# Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero

Chichewa: Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero (Bible) of Malawi

# Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero

## Chichewa: Biblica® Tsekulani Mawu a Mulungu mu Chichewa Chalero (Bible) of Malawi

copyright © 2016 Biblica, Inc.

Language: Chichewa

Contributor: Biblica, Inc.

Biblica® Open God's Word in Contemporary Chichewa™
Copyright © 2002, 2016 by Biblica, Inc.
"Biblica" is a trademark registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc. Used with permission.
Used with permission. All rights reserved worldwide.
All content on open.bible is made available under a Creative Commons Attribution-ShareAlike 4.0 License (http://creativecommons.org/licenses/by-sa/4.0/).
You are free to:

Share — copy and redistribute the material in any medium or format

Adapt — remix, transform, and build upon the material for any purpose, even commercially

Under the following conditions:

Attribution — You must attribute the work as follows: "Original work available for free at www.biblica.com and open.bible" Attribution statements in derivative works should not in any way suggest that we endorse you or your use of this work.

ShareAlike — If you remix, transform, or build upon the material, you must distribute your contributions under the same license as the original.

Use of trademarks: Biblica® is a trademark registered in the United States Patent and Trademark Office by Biblica, Inc. and may not be included on any derivative works. Unaltered content from open.bible must include the Biblica® trademark when distributed to others. If you alter the content in any way, you must remove the Biblica® trademark before distributing your work.
This translation is made available to you under the terms of the Creative Commons Attribution Share-Alike license 4.0.
You have permission to share and redistribute this Bible translation in any format and to make reasonable revisions and adaptations of this translation, provided that:

You include the above copyright and source information.

If you make any changes to the text, you must indicate that you did so in a way that makes it clear that the original licensor is not necessarily endorsing your changes.

If you redistribute this text, you must distribute your contributions under the same license as the original.

Pictures included with Scriptures and other documents on this site are licensed just for use with those Scriptures and documents. For other uses, please contact the respective copyright owners.
Note that in addition to the rules above, revising and adapting God's Word involves a great responsibility to be true to God's Word. See Revelation 22:18-19.

2021-11-15

---

PDF generated using Haiola and XeLaTeX on 21 Feb 2024 from source files dated 16 Nov 2021
f540eb34-4377-5601-9dcf-0a053d172faa

Contents

GENESIS . . . 1
EKSODO . . . 75
LEVITIKO . . . 133
NUMERI . . . 176
DEUTERONOMO . . . 237
YOSWA . . . 287
OWERUZA . . . 321
RUTE . . . 356
1 SAMUELI . . . 361
2 SAMUELI . . . 406
1 MAFUMU . . . 446
2 MAFUMU . . . 492
1 MBIRI . . . 536
2 MBIRI . . . 584
EZARA . . . 633
NEHEMIYA . . . 649
ESTERE . . . 672
YOBU . . . 683
MASALIMO . . . 734
MIYAMBO . . . 871
MLALIKI . . . 923
NYIMBO YA SOLOMONI . . . 937
YESAYA . . . 947
YEREMIYA . . . 1053
MALIRO . . . 1149
EZEKIELI . . . 1162
DANIELI . . . 1237
HOSEYA . . . 1259
Yoweli . . . 1276
AMOSI . . . 1283
OBADIYA . . . 1296
YONA . . . 1298
MIKA . . . 1301
NAHUMU . . . 1311
HABAKUKU . . . 1316
ZEFANIYA . . . 1321
HAGAI . . . 1326
ZEKARIYA . . . 1329
MALAKI . . . 1342
MATEYU . . . 1346
MARKO . . . 1395
LUKA . . . 1426
YOHANE . . . 1478

MACHITIDWE A ATUMWI . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1517
AROMA . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1565
1 AKORINTO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1587
2 AKORINTO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1607
AGALATIYA . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1621
AEFESO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1628
AFILIPI . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1635
AKOLOSE . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1641
1 ATESALONIKA . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1646
2 ATESALONIKA . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1650
1 TIMOTEYO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1653
2 TIMOTEYO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1659
TITO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1663
FILEMONI . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1666
AHEBRI . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1668
YAKOBO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1684
1 PETRO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1690
2 PETRO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1696
1 YOHANE . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1700
2 YOHANE . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1706
3 YOHANE . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1707
YUDA . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1708
CHIVUMBULUTSO . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . . 1710

# Genesis

*Chiyambi cha Chilengedwe*

1 Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi.
2 Dziko lapansi linali losakonzedwa ndi lopanda kanthu. Mdima wandi-
weyani unakuta nyanja ndipo Mzimu wa Mulungu unkayendayenda
pamwamba pa madziwo.

3 Pamenepo Mulungu anati, "Kuwale" ndipo kunawaladi. 4 Mulungu
anaona kuti kuwalako kunali bwino ndipo Iye analekanitsa kuwala
ndi mdima. 5 Mulungu anatcha kuwalako "usana" ndipo mdima
anawutcha "usiku." Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku
loyamba.
6 Kenaka Mulungu anati, "Pakhale thambo pakati pa madzi kuti
lilekanitse madzi a m'mwamba ndi madzi a pansi." 7 Ndipo
Mulungu anapanga thambo nalekanitsa madzi amene anali pansi ndi
pamwamba pa thambo lija, ndipo zinachitikadi. 8 Mulungu anatcha
thambo lija "kumwamba." Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa
pa tsiku lachiwiri.
9 Mulungu anati, "Madzi a pansi pa thambo asonkhane pa malo
amodzi kuti mtunda uwoneke," ndipo zinachitikadi. 10 Mulungu
anawutcha mtundawo "dziko," madzi osonkhana pamodziwo
anawatcha "nyanja." Ndipo Mulungu anaona kuti zinali bwino.
11 Kenaka Mulungu anati, "Dziko libereke zomera zobala mbewu,
mitengo yobala zipatso za mbewu, molingana ndi mitundu yake." Ndipo
zinachitikadi. 12 Dziko linabereka zomera zokhala ndi mbewu monga
mwa mitundu yake ndi mitengo yokhala ndi zipatso za mbewu m'kati
mwake monga mwa mitundu yake. Ndipo Mulungu anaona kuti zinali
bwino. 13 Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku lachitatu.
14 Mulungu anati, "Pakhale zowunikira kuthambo kuti zilekanitse usana
ndi usiku. Ndipo zimenezi zikhale zizindikiro zoonetsa nyengo,
masiku ndi zaka; 15 zikhale kuthambo kuti ziwunikire pa dziko
lapansi. Ndipo zinachitikadi." 16 Mulungu anapanga zowunikira
zazikulu ziwiri; chachikulu chilamulire usana ndi chaching'ono
chilamulire usiku. Iye anapanganso nyenyezi. 17 Mulungu anaziyika
mlengalenga kuti ziziwunikira pa dziko lapansi, 18 kuti zilamulire
usana ndi usiku, ndi kuti zilekanitse kuwala ndi mdima. Mulungu
anaona kuti zinali bwino. 19 Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa
pa tsiku lachinayi.
20 Mulungu anati, "M'madzi mukhale zamoyo zochuluka ndipo mbalame
ziwuluke mlengalenga pamwamba pa dziko lapansi." 21 Choncho
Mulungu analenga zamoyo zikuluzikulu za m'nyanja ndi chamoyo
chamtundu uliwonse chokhala m'madzi ndi mbalame iliyonse ya
mapiko monga mwa mtundu wake. Mulungu anaona kuti zinali
bwino. 22 Mulungu anazidalitsa nati, "Muswane, ndi kudzaza m'madzi
a m'nyanja, ndipo mbalame zichuluke pa dziko lapansi." 23 Ndipo
panali madzulo ndiponso mmawa pa tsiku lachisanu.
24 Kenaka Mulungu anati, "Dziko lapansi litulutse zolengedwa zamoyo
monga mwa mitundu yawo: ziweto, zolengedwa zokwawa ndi nyama

zakuthengo, iliyonse monga mwa mtundu wake." Ndipo zinaterodi.
25 Mulungu anapanga nyama zakuthengo monga mwa mitundu yawo, nyama zoweta monga mwa mitundu yawo ndi nyama zokwawa monga mwa mitundu yawo. Ndipo Mulungu anaona kuti zinali bwino.
26 Zitatha izi Mulungu anati, "Tipange munthu m'chifanizo chathu, mofanana ndi ife kuti alamulire nsomba za m'nyanja, mbalame zamlengalenga, nyama zonse zoweta ndi zonse zokwawa za pa dziko lapansi ndi zamoyo zonse zakutchire."

27 Ndipo Mulungu analenga munthu m'chifanizo chake.
Anawalengadi m'chifanizo cha Mulungu;
analenga iwo, mwamuna ndi mkazi.

28 Mulungu anawadalitsa nati kwa iwo, "Muberekane, muchulukane, mudzaze dziko lapansi ndipo muligonjetse. Mulamulire nsomba zam'nyanja, mbalame zamlengalenga ndi cholengedwa chamoyo chilichonse chimene chimayenda mokwawa pa dziko lapansi."
29 Kenaka Mulungu anati, "Ine ndakupatsani chomera chilichonse cha pa dziko lapansi chimene chili ndi mbewu komanso mtengo uliwonse wobala zipatso zokhala ndi mbewu m'kati mwake kuti zikhale
chakudya chanu. 30 Ndaperekanso msipu kwa nyama zonse za pa
dziko lapansi ndi kwa mbalame zamlengalenga ndi kwa cholengedwa chamoyo chilichonse chimene chimakwawa, chilichonse chimene chili ndi moyo." Ndipo zinachitikadi.
31 Mulungu anaona zonse zimene anazilenga kuti zinali zabwino kwambiri. Ndipo panali madzulo ndiponso mmawa, tsiku lachisanu ndi chimodzi.

# 2

1 Motero kumwamba, dziko lapansi ndi zonse za m'menemo zinatha kulengedwa monga mwa kuchuluka kwawo.

2 Pofika tsiku lachisanu ndi chiwiri Mulungu anamaliza ntchito zonse zimene ankagwira ndipo pa tsiku lachisanu ndi chiwiri anapumula
ku ntchito zake zonse. 3 Ndipo Mulungu anadalitsa tsiku lachisanu
ndi chiwiri nalipatula, chifukwa pa tsiku limeneli Iye anapumula ku ntchito yonse yolenga imene anayigwira.

### *Adamu ndi Hava*

4 Mbiri ya momwe kumwamba ndi dziko lapansi zinalengedwera pa tsiku lija Yehova Mulungu ankazilenga ndi iyi:

Yehova Mulungu atapanga dziko lapansi ndi kumwamba, 5 zitsamba
zinali zisanamere ndipo chomera chilichonse chinali chisanamerenso popeza Yehova Mulungu anali asanagwetse mvula pa dziko lapansi.
Panalibe munthu wolima nthaka, 6 koma kasupe ankatuluka m'nthaka ndi
kuthirira pa dziko lonse. 7 Tsono Yehova Mulungu anawumba munthu
kuchokera ku dothi nawuziramo mpweya wamoyo m'mphuno mwake ndipo munthuyo anakhala wamoyo.
8 Kenaka Yehova Mulungu anatsekula munda wa Edeni chakummawa;
kumeneko anayikako munthu amene anamupanga uja. 9 Ndipo Yehova
Mulungu anameretsa m'mundamo mitengo ya mitundu yonse. Inali mitengo yokongola ndi ya zipatso zokoma. Pakati pa munda uja panali

mtengo wopatsa moyo ndi mtengo wopatsa nzeru zodziwitsa chabwino ndi choyipa.

10 Mtsinje wothirira mundawo unkatuluka mu Edeni; kuchokera apo unkagawikana kukhala mitsinje inayi. 11 Dzina la mtsinje woyamba ndi Pisoni; uwu umazungulira dziko lonse la Havila, kumene kuli golide. 12 (Golide wa ku dziko ili ndi wabwino. Kulinso miyala yokongola ya bedola ndi onikisi). 13 Dzina la mtsinje wachiwiri ndi Gihoni; uwu umazungulira dziko lonse la Kusi. 14 Dzina la mtsinje wachitatu ndi Tigirisi; umayenda chakummawa kwa Asiriya. Ndipo mtsinje wachinayi ndi Yufurate.

15 Yehova Mulungu anatenga munthu uja ndi kumuyika m'munda wa Edeni kuti awulime ndi kuwusamalira. 16 Ndipo Yehova Mulungu analamula munthu uja kuti, "Uzidya zipatso za mu mtengo wina uliwonse m'mundamu; 17 koma usadye zipatso za mu mtengo wodziwitsa chabwino ndi choyipa, popeza ukadzadya za mu mtengowu udzafa ndithu."

18 Ndipo Yehova Mulungu anati, "Sibwino kuti munthu akhale yekha. Ndidzamupangira mnzake womuthandiza."

19 Kenaka Yehova Mulungu anawumba ndi dothi nyama zonse zakuthengo ndi mbalame zonse zamlengalenga. Ndipo Iye anapita nazo kwa munthu uja kuti akazipatse mayina; ndipo dzina lililonse limene Adamu anapereka ku chamoyo chilichonse, lomwelo linakhala dzina lake. 20 Choncho Adamu anazitcha mayina ziweto zonse, mbalame zamlengalenga ndi nyama zakuthengo zonse.

Komabe munthu uja analibe mnzake womuthandiza. 21 Tsono Yehova Mulungu anamugonetsa munthu uja tulo tofa nato; ali mtulo chomwecho, Mulungu anachotsa imodzi mwa nthiti zake ndi kutseka pamalopo ndi mnofu. 22 Motero Yehova Mulungu anapanga mkazi ndi nthiti ija imene anatenga kwa munthu uja nabwera naye kwa iye.

23 Munthu uja anati,

"Uyu ndiye fupa lochokera ku mafupa anga
  ndi mnofu wochokera ku mnofu wanga;
adzatchedwa 'mkazi,'
  popeza wachokera mwa mwamuna."

24 N'chifukwa chake, mwamuna amasiya abambo ndi amayi ake nakaphatikana ndi mkazi wake ndipo awiriwo amakhala thupi limodzi.

25 Munthu uja ndi mkazi wakeyo, onse awiri anali maliseche ndipo analibe manyazi.

# 3

*Kuchimwa kwa Munthu*

1 Ndipo njoka inali yochenjera kuposa nyama yakuthengo iliyonse imene Yehova Mulungu anapanga. Njokayo inati kwa mkaziyo, "Kodi Mulungu ananenadi kuti, 'Inu musadye zipatso za mtengo uliwonse m'mundamu?' "

2 Mkaziyo anati kwa njokayo, "Tikhoza kudya zipatso za m'mitengo ya m'mundawu, 3 koma Mulungu anati, 'Musadye zipatso za mu mtengo umene uli pakati pa munda, ndipo musadzawukhudze kuti mungadzafe.' "

4 "Ndithudi simudzafa," inatero njokayo kwa mkaziyo. 5 "Pakuti Mulungu akudziwa kuti tsiku limene mudzadye zipatso za mu mtengowo, maso anu adzatsekuka, ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wodziwa zabwino ndi zoyipa."

6 Pamene mkaziyo anaona kuti mtengowo unali wabwino kudya ndi
wokongola ndi kuti unali wopatsa nzeru, anatengako zipatso zake nadya.
Zina anamupatsako mwamuna wake amene anali naye pomwepo ndipo
naye anadyanso. 7 Kenaka maso awo anatsekuka, ndipo anazindikira
kuti anali maliseche. Choncho anasoka masamba a mkuyu nadzipangira
zovala.

8 Kenaka munthu uja ndi mkazi wake anamva mtswatswa wa Yehova
Mulungu akuyendayenda m'mundamo madzulo a tsikulo, ndipo iwo
anabisala pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'mundamo.
9 Yehova Mulungu anayitana munthu uja kuti, "Uli kuti?"

10 Iye anayankha, "Ndinakumvani m'mundamo, ndipo ndimaopa chifukwa ndinali maliseche; choncho ndinabisala."

11 Ndipo anamufunsa, "Ndani anakuwuza kuti uli maliseche? Kodi wadya zipatso za mtengo umene ndinakulamulira kuti usadye?"

12 Koma munthu uja anati, "Mkazi amene munandipatsa kuti ndizikhala nayeyu anandipatsako chipatso cha mtengowo ndipo ndinadya."

13 Tsono Yehova Mulungu anati kwa mkaziyo, "Wachitachi n'chiyani?"

Mkaziyo anati, "Njoka inandinamiza, ndipo ndinadya."

14 Choncho Yehova Mulungu anati kwa njokayo, "Popeza wachita zimenezi,

"Ndiwe wotembereredwa kuposa ziweto zonse
    ndi nyama zakuthengo zonse.
Udzayenda chafufumimba
    ndipo udzadya fumbi
    masiku onse a moyo wako.
15 Ndipo ndidzayika chidani
    pakati pa iwe ndi mkaziyo,
    pakati pa mbewu yako ndi mbewu yake;
Iye adzaphwanya mutu wako
    ndipo iwe udzaluma chidendene chake."

16 Kwa mkaziyo Iye anati,

"Ndidzachulukitsa ululu wako kwambiri pamene uli ndi pakati;
    ndipo udzamva ululu pa nthawi yako yobereka ana.
Udzakhumba mwamuna wako,
    ndipo adzakulamulira."

17 Ndipo kwa Adamu Mulungu anati, "Chifukwa wamvera mkazi wako ndipo wadya zipatso za mu mtengo umene ndinakulamulira kuti, 'Usadye.'

"Nthaka yatembereredwa chifukwa cha iwe,
    movutikira udzadya zochokera m'nthakamo
    masiku onse a moyo wako.
18 M'nthakamo mudzamera minga ndi nthula
    ndipo udzadya zomera zakuthengo.
19 Kuti upeze chakudya udzayenera
    kukhetsa thukuta,
mpaka utabwerera ku nthaka
    pakuti unachokera kumeneko;
pakuti ndiwe fumbi
    ku fumbi komweko udzabwerera."

20 Munthu uja anatcha mkazi wake Hava, chifukwa iyeyu adzakhala mayi wa anthu onse amoyo.

21 Yehova Mulungu anapangira Adamu ndi mkazi wake zovala zachikopa
ndipo anawaveka. 22 Ndipo Yehova Mulungu anati, "Tsopano munthu

uyu wasanduka mmodzi wa ife, wodziwa zabwino ndi zoyipa. Iyeyu
asaloledwe kutambasula dzanja ndi kutengako zipatso za mu mtengo
wopatsa moyo uja kuti angakhale ndi moyo mpaka muyaya.” 23 Kotero
Yehova Mulungu anatulutsa Adamu M’munda wa Edeni kuti azilima
m’nthaka imene anachokera. 24 Atamuthamangitsa munthu uja, Yehova
anayika Akerubi mbali ya kummawa kwa Munda wa Edeni ndi lupanga
lamoto limene limayendayenda ponsepo, kuteteza njira ya ku mtengo
wopatsa moyo.

# 4

### *Kaini ndi Abele*

1 Adamu anagona malo amodzi ndi Hava mkazi wake ndipo mkaziyo
anakhala woyembekezera nabala Kaini, ndipo anati, “Ndi thandizo la
Yehova ndapeza mwana wamwamuna.” 2 Kenaka anabereka m’bale wake
Abele.

Abele anali woweta nkhosa ndipo Kaini anali mlimi. 3 Patapita nthawi,
Kaini anatenga zipatso za ku munda nakazipereka kwa Yehova monga
nsembe. 4 Nayenso Abele anatenga ana ankhosa oyamba kubadwa
pamodzi ndi mafuta ake nakazipereka ngati nsembe kwa Yehova. Yehova
anakondwera ndi Abele ndi nsembe yake. 5 Koma sanakondwere ndi Kaini
ndi nsembe yake. Kotero Kaini anakwiya kwambiri ndipo nkhope yake
inagwa.

6 Choncho Yehova anati kwa Kaini, “Chifukwa chiyani wakwiya ndipo
bwanji nkhope yako yagwa? 7 Ukanachita zabwino sindikanakulandira
kodi? Koma tsopano wachita zoyipa ndipo tchimo likukudikira pa khomo
pako, likufuna kukugwira; koma iwe uyenera kugonjetsa tchimolo.”

8 Tsiku lina Kaini anati kwa m’bale wake Abele, “Tiye tipite ku munda.”
Ndipo ali ku mundako, Kaini anawukira m’bale wake namupha.

9 Ndipo Yehova anamufunsa Kaini kuti, “Ali kuti m’bale wako Abele?”

Iye anayankha kuti, “Sindikudziwa. Kodi ine ndine wosunga m’bale
wanga?”

10 Yehova anati, “Kodi wachita chiyani? Tamvera! Magazi a m’bale
wako akulirira kwa Ine kuchokera m’nthaka. 11 Ndipo tsopano ndiwe
wotembereredwa ndipo wachotsedwa m’dziko limene nthaka yake inat-
sekula pakamwa pake kulandira magazi a m’bale wako amene unakhetsa.
12 Udzalima munda koma nthakayo sidzakupatsanso zokolola zake. Udza-
khala wosakhazikika; womangoyendayenda pa dziko lapansi.”

13 Kaini anati kwa Yehova, “Chilango changa ndi chachikulu kuposera
mphamvu zanga. 14 Lero mukundipirikitsa pa dziko ndi pamaso
panu; ndidzakhala wosakhazikika, woyendayenda, ndipo aliyense amene
adzandipeze adzandipha.”

15 Koma Yehova anamuwuza kuti, “Sizidzatero ayi; aliyense amene
adzaphe Kaini adzalangidwa ndi kulipiritsidwa kasanu ndi kawiri.”
Pamenepo Yehova anayika chizindikiro pa Kaini kuti aliyense womupeza
asamuphe. 16 Ndipo Kaini anachoka pamaso pa Yehova nakakhala ku
dziko la Nodi, kummawa kwa Edeni.

### *Banja la Kaini*

17 Kaini anagona malo amodzi ndi mkazi wake ndipo mkaziyo anakhala
woyembekezera nabala Enoki. Kaini nthawi imeneyo n’kuti akumanga
mzinda ndipo anawutcha dzina la mwana wake Enoki. 18 Enoki anabereka

Iradi; Iradi anabereka Mehuyaeli, ndipo Mehuyaeli anabereka Metusela, ndipo Metusela anabereka Lameki.

[19] Lameki anakwatira akazi awiri, wina dzina lake linali Ada ndi winayo
dzina lake linali Zila. [20] Ada anabereka Yabala; iyeyu anali kholo la onse
okhala m'matenti ndi oweta ziweto. [21] Dzina la m'bale wake linali Yubala;
iyeyu anali kholo la onse oyimba zeze ndi chitoliro. [22] Zila nayenso anali
ndi mwana wamwamuna, dzina lake Tubala-Kaini. Iyeyu anali kholo la
amisiri onse osula zida za mkuwa ndi chitsulo. Mlongo wake wa Tubala-
Kaini anali Naama.

[23] Lameki anawuza akazi akewo kuti,
"Ada ndi Zila, ndimvereni;
inu akazi anga imvani mawu anga.
Ine ndinapha munthu chifukwa anandipweteka.
Ndinapha mnyamatayo chifukwa anandimenya.
[24] Ngati wopha Kaini amulipsira kasanu n'kawiri,
ndiye kuti wopha ine Lameki adzamulipsira kokwanira 77."

[25] Adamu anagonanso malo amodzi ndi mkazi wake, ndipo anabereka
mwana wamwamuna namutcha Seti, kutanthauza kuti, "Mulungu wandi-
patsa mwana wina m'malo mwa Abele, popeza Kaini anamupha." [26] Seti
naye anali ndi mwana wa mwamuna, ndipo anamutcha Enosi.

Pa nthawi imeneyi anthu anayamba kupemphera m'dzina la Yehova.

# 5

*Mibado Kuyambira pa Adamu Mpaka Nowa*

[1] Ndondomeko ya mibado ya Adamu ndi iyi:

Pamene Mulungu analenga munthu, anamulenga m'chifaniziro cha
Mulungu. [2] Iye analenga mwamuna ndi mkazi. Anawadalitsa ndipo
anawatcha "Munthu."

[3] Pamene Adamu anali ndi zaka 130, anabereka mwana wamwamuna
wofanana naye ndipo anamutcha Seti. [4] Atabadwa Seti, Adamu anakhala
ndi moyo zaka zina 800 ndipo anabereka ana ena aamuna ndi aakazi.
[5] Zaka zonse za Adamu zinali 930 ndipo anamwalira.

[6] Pamene Seti anali ndi zaka 105, anabereka Enosi. [7] Atabadwa Enosi,
Seti anakhala ndi moyo zaka zina 807 ndipo anabereka ana ena aamuna
ndi aakazi. [8] Zaka zonse za Seti zinali 912 ndipo anamwalira.

[9] Pamene Enosi anali ndi zaka 90, anabereka Kenani. [10] Atabadwa
Kenani, Enosi anakhala ndi moyo zaka zina 815 ndipo anabereka ana
ena aamuna ndi aakazi. [11] Zaka zonse za Enosi pamodzi zinali 905 ndipo
anamwalira.

[12] Pamene Kenani anali ndi zaka 70, anabereka Mahalaleli. [13] Atabadwa
Mahalaleli, Kenani anakhala ndi moyo zaka zina 840 ndipo anabereka
ana ena aamuna ndi aakazi. [14] Zaka zonse za Kenani zinali 910, ndipo
anamwalira.

[15] Pamene Mahalaleli anali ndi zaka 65, anabereka Yaredi. [16] Atabadwa
Yaredi, Mahalaleli anakhala ndi moyo zaka zina 830 ndipo anabereka ana
ena aamuna ndi aakazi. [17] Zaka zonse za Mahalaleli zinali 895 ndipo
anamwalira.

[18] Pamene Yaredi anali ndi zaka 162, anabereka Enoki. [19] Atabadwa
Enoki, Yaredi anakhala ndi moyo zaka zina 800 ndipo anabereka ana ena
aamuna ndi aakazi. [20] Zaka zonse za Yaredi zinali 962 ndipo anamwalira.

21 Pamene Enoki anali ndi zaka 65, anabereka Metusela. 22 Atabadwa
Metusela, Enoki anayenda ndi Mulungu zaka 300 ndipo anabereka ana ena
aamuna ndi aakazi. 23 Zaka zonse za Enoki zinali 365. 24 Enoki anayenda
ndi Mulungu; ndipo iye sanaonekenso chifukwa Mulungu anamutenga.

25 Pamene Metusela anali ndi zaka 187, anabereka Lameki. 26 Ndipo
atabadwa Lameki, Metusela anakhala ndi moyo zaka zina 782 ndipo
anabereka ana ena aamuna ndi aakazi. 27 Zaka zonse za Metusela zinali
969, ndipo anamwalira.

28 Pamene Lameki anali ndi zaka 182, anabereka mwana wamwamuna.
29 Ndipo anamutcha Nowa ndipo anati, “Iyeyu adzatipumulitsa ku
ntchito zathu zolemetsazi, zolima nthaka imene Yehova anayitemberera.”
30 Atabadwa Nowa, Lameki anakhala zaka zina 595 ndipo anabereka ana
ena aamuna ndi aakazi. 31 Zaka zonse za Lameki zinali 777, ndipo kenaka
anamwalira.

32 Pamene Nowa anali ndi zaka 500, anabereka Semu, Hamu ndi Yafeti.

# 6

### *Kuyipa kwa Mtundu wa Anthu*

1 Anthu atayamba kuchuluka pa dziko lapansi ndi kubereka ana aakazi,
2 ana aamuna a Mulungu anaona kuti ana aakazi a anthuwo anali
okongola. Ndipo anakwatira aliyense amene anamusankha. 3 Tsono
Yehova anati, “Sindilola kuti chipwirikiti chikuchitikachi chipitirire mpaka
muyaya, pakuti iye ndi munthu; masiku a moyo wake adzakhala zaka
120.”

4 Masiku amenewo komanso pambuyo pake, pa dziko lapansi panali
Anefili, anthu amphamvu ndiponso otchuka. Anthuwa ndi amene
ankabadwa ana a Mulungu aja atakwatira ana aakazi a anthu.

5 Pamene Yehova anaona kuti kuyipa kwa munthu pa dziko lapansi
kunali kwakukulu ndi kuti nthawi zonse amalingalira ndi kukhumbira
kuchita zoyipa zokhazokha, 6 Yehova anamva chisoni kuti analenga
munthu ndi kumuyika pa dziko lapansi, ndipo anawawidwa mtima.
7 Choncho Yehova anati, “Ndidzafafaniza munthu, nyama, zonse zokwawa,
ndi mbalame za mu mlengalenga pa dziko lapansi, pakuti ndikumva
chisoni kuti ndinazilenga zimenezi.” 8 Koma Yehova anamukomera mtima
Nowa.

### *Nowa ndi Chigumula*

9 Mbiri ya Nowa inali yotere:

Nowa anali munthu wolungama ndi wopanda tchimo pakati pa anthu
a m’bado wake. Ndipo anayenda ndi Mulungu. 10 Nowa anabereka ana
aamuna atatu: Semu, Hamu ndi Yafeti.

11 Chiwawa chinadzaza pa dziko lapansi kotero kuti dziko linakhala
lowononongeka pamaso pa Mulungu. 12 Mulungu atayang’ana, anaona
kuti dziko layipadi chifukwa cha makhalidwe oyipa a anthu onse pa
dziko lapansi. 13 Ndipo Mulungu anati kwa Nowa, “Ndatsimikiza mtima
kuti ndiwononge anthu onse, pakuti dziko lapansi ladzaza ndi ntchito
zawo zoyipa. Ndithudi ndiwawononga pamodzi ndi zonse za pa dziko.
14 Tsono udzipangire chombo cha matabwa a mtengo wanjale; m’kati
mwake upange zipinda ndipo upake phula m’kati ndi kunja. 15 Uchipange
motere: Chombo chikhale mamita 140 mulitali, mamita 23 mulifupi ndi

mamita 13 mu msinkhu wake. 16 Uchipangire denga ndi kuchimaliza
ndi zenera la masentimita makumi asanu. Uyike khomo m'mbali mwa
chombocho ndi kupanga zipinda zosanjikana; chapansi, chapakati ndi
chapamwamba. 17 Ndidzagwetsa mvula ya chigumula pa dziko lapansi
kuti ndiwononge zamoyo zonse za pansi pa thambo ndipo chilichonse cha
pa dziko lapansi chidzafa. 18 Koma ndidzachita pangano langa ndi iwe.
Iwe, ana ako aamuna, mkazi wako ndi akazi a ana ako nonse mudzalowa
m'chombocho. 19 Iwe udzalowa m'chombocho ndi zolengedwa zamoyo
zonse ziwiriziwiri, chachimuna ndi chachikazi, kuti zisungike ndi moyo
pamodzi ndi iwe. 20 Udzatenga ziwiriziwiri za mitundu yonse ya mbalame,
mitundu yonse ya nyama, ndi mitundu yonse ya zokwawa kuti zikhale ndi
moyo. 21 Udzatengenso chakudya cha mtundu uliwonse ndi kuchisunga
kuti inu ndi nyamazo muzidzadya."

22 Nowa anachita zonse monga Mulungu anamulamulira.

# 7

1 Ndipo Yehova anati kwa Nowa, "Lowa mu chombo iwe ndi banja lako
lonse, chifukwa ndaona kuti ndiwe wolungama mu m'bado uwu. 2 Pa
mtundu uliwonse wa nyama zoti n'kudya utengepo zazimuna zisanu ndi
ziwiri ndi zazikazi zisanu ndi ziwirinso. Koma pa mtundu wa nyama
iliyonse yosati n'kudya utengepo zazimuna ziwiri ndi zazikazi ziwirinso.
3 Chimodzimodzinso mbalame, utenge zisanu ndi ziwiri zazimuna ndi
zisanu ndi ziwiri zazikazi za mtundu uliwonse kuti mitundu yawo
isungike ndi moyo pa dziko lonse lapansi. 4 Pakapita masiku asanu ndi
awiri ndidzagwetsa mvula pa dziko lapansi kwa masiku makumi anayi
usana ndi usiku ndipo ndidzawononga cha moyo chilichonse chimene
ndinachipanga pa dziko lapansi."

5 Ndipo Nowa anachita zonse zimene Yehova anamulamulira.

6 Pamene chigumula chinabwera pa dziko lapansi Nowa anali ndi zaka
600. 7 Ndipo Nowa, ana ake aamuna, mkazi wake, pamodzi ndi ana ake
aakazi analowa mu chombo chija kuthawa madzi a chigumula. 8 Nyama
zoti n'kudya ndi nyama zosadyedwa, mbalame, pamodzi ndi nyama
zokwawa zonse zinadza kwa Nowa ziwiriziwiri ndi kulowa m'chombomo.
9 Ndipo Nowa anatenga ziwiriziwiri, yayimuna ndi yayikazi monga
anamulamulira Mulungu. 10 Patapita masiku asanu ndi awiri chigumula
chinabwera pa dziko lapansi.

11 Pa tsiku la 17 la mwezi wachiwiri, Nowa ali ndi zaka 600, akasupe
onse akuya kwambiri anasefuka ndiponso zitseko za madzi akumwamba
zinatsekuka. 12 Ndipo mvula inagwa pa dziko lapansi masiku makumi
anayi usana ndi usiku.

13 Linali tsiku lomwelo pamene Nowa ndi ana ake aamuna, Semu, Hamu
ndi Yafeti, pamodzi ndi mkazi wake ndi akazi a ana ake atatu aja analowa
mu chombo. 14 Iwowa analowa m'chombomo pamodzi ndi nyama iliyonse
ya kutchire monga mwa mtundu wake, ziweto zonse monga mwa mitundu
yawo, nyama yokwawa iliyonse monga mwa mtundu wake ndi mbalame
iliyonse monga mwa mtundu wake. 15 Nowa analowa mu chombo muja
pamodzi ndi zamoyo zonse. 16 Iye analowa nazo zazimuna ndi zazikazi
monga mmene Mulungu anamulamulira. Kenaka Yehova anatseka pa
khomo.

17 Chigumula chinagwa pa dziko la pansi kwa masiku makumi
anayi. Madzi anayamba kuchuluka ndipo ananyamula chombo chija ndi

kuchiyandamitsa pamwamba pa dziko. 18 Madzi anafika mwamphamvu
ndipo anachulukirachulukira pa dziko lapansi moti chombo chinayan-
dama pamwamba pa madziwo. 19 Madzi a chigumula anabwerabe
molimbika motero kuti mapiri ataliatali onse a pa dziko anamizidwa.
20 Madzi anakwera namiza mapiri kwa mamita pafupifupi asanu ndi awiri.
21 Chamoyo chilichonse choyenda pa dziko lapansi chinafa: mbalame,
ziweto, nyama zakuthengo, miyandamiyanda ya zonse zolengedwa za
pa dziko lapansi pamodzi ndi anthu. 22 Chilichonse chamoyo, chokhala
pa mtunda chinafa. 23 Chamoyo chilichonse pa dziko lapansi china-
wonongedwa, kuyambira munthu, nyama, zokwawa ndi mbalame. Nowa
yekha ndiye anatsala pamodzi ndi onse amene anali naye.

24 Madziwo anadzaza dziko lonse lapansi kwa masiku 150.

# 8

*Nowa Atuluka M'chombo*

1 Tsono Mulungu anakumbukira Nowa ndi nyama zonse zakuthengo ndi
ziweto zimene anali nazo mu chombo. Yehova anatumiza mphepo pa
dziko lapansi ndipo madzi anaphwera. 2 Tsono akasupe a madzi ambiri
a pansi pa dziko ndi zitseko za madzi a kumwamba zinatsekedwa, ndipo
mvula inaleka kugwa. 3 Madzi amaphwabe pa dziko lapansi. Pakutha pa
masiku 150, madzi anatsika, 4 ndipo pa tsiku la 17 la mwezi wachisanu
ndi chiwiri, chombo chija chinakakhazikika pa mapiri a Ararati. 5 Madzi
anapitirira kuphwa mpaka mwezi wa khumi, ndipo pa tsiku loyamba la
mwezi wa khumiwo msonga za mapiri zinayamba kuonekera.

6 Patapita masiku makumi anayi, Nowa anatsekula zenera limene
anapanga m'chombomo 7 natulutsa khwangwala, koma khwangwalayo
ankangowuluka uku ndi uku mpaka madzi anawuma pa dziko lapansi.
8 Kenaka anatulutsa nkhunda kuti aone ngati madzi aphwa pa dziko.
9 Koma nkhunda sinapeze poti n'kutera chifukwa panali madzi ponse-
ponse pa dziko lapansi. Choncho inabwerera kwa Nowa m'chombo.
Nowa anatulutsa dzanja lake kunja ndi kutenga nkhundayo kuyibwezera
m'chombo mmene iye anali. 10 Choncho anadikirabe masiku ena asanu
ndi awiri ndipo anatulutsanso nkhundayo m'chombo muja. 11 Pamene
nkhunda inabwerera madzulo ake, inali itanyamula tsamba laliwisi la
mtengo wa olivi. Motero Nowa anadziwa kuti madzi aphwadi pa dziko
lapansi. 12 Iye anadikira masiku ena asanu ndi awiri ndipo anatumizanso
nkhunda ija, koma nthawi imeneyi sinabwererenso kwa iye.

13 Pofika tsiku loyamba la mwezi woyamba wa chaka chimene Nowa
anakwanitsa zaka 601, madzi anawuma pa dziko lapansi. Ndipo
Nowa anachotsa denga la chombo ndipo anaona kuti kunja kwawuma.
14 Pokwana tsiku la 27 la mwezi wachiwiri dziko lapansi linawumiratu.

15 Tsono Mulungu anawuza Nowa kuti, 16 "Iwe, mkazi wako, ana ako
pamodzi ndi akazi awo tulukani m'chombomo. 17 Tulutsa zamoyo zonse
zili ndi iwe, mbalame, nyama ndi zokwawa zonse kuti ziswane ndi
kuchulukana pa dziko lapansi."

18 Nowa anatuluka pamodzi ndi ana ake aamuna, mkazi wake ndi akazi
a ana ake. 19 Nyama zonse, zokwawa zonse, mbalame zonse, chilichonse
choyenda pa dziko lapansi, zinatuluka m'chombo motsogozana monga
mwa mitundu yawo.

20 Pamenepo Nowa anamanga guwa lansembe la Yehova ndipo anaten-
gako mtundu uliwonse wa nyama zoti n'kudya ndi mbalame zoti n'kudya

naperekapo nsembe yopsereza. 21 Yehova atamva fungo labwino anati
mu mtima mwake: “Sindidzatembereranso nthaka chifukwa cha munthu,
ngakhale kuti maganizo a mu mtima mwake ndi oyipa kuyambira ubwana
wake. Ndipo sindidzawononganso zolengedwa zonse zamoyo monga
ndachitiramu.
22 “Nthawi zonse mmene dziko lapansi lidzakhalire,
nthawi yodzala ndi nthawi yokolola
yozizira ndi yotentha,
dzinja ndi chilimwe,
usana ndi usiku,
sizidzatha.”

# 9

*Pangano la Mulungu ndi Nowa*

1 Ndipo Mulungu anadalitsa Nowa ndi ana ake aamuna nati kwa iwo,
“Berekanani ndipo muchulukane ndi kudzaza dziko lapansi. 2 Nyama
zonse za dziko lapansi, ndi mbalame zonse za mlengalenga, ndi chamoyo
chilichonse chokwawa, ndiponso nsomba zonse za ku nyanja; zidza-
kuopani ndipo ndazipereka kuti muzilamulire. 3 Tsopano chamoyo chili-
chonse chidzakhala chakudya chanu. Monga momwe ndinakupatsirani
ndiwo zamasamba, tsopano ndikupatsaninso nyama iliyonse.

4 “Koma musamadye nyama imene ikanali ndi magazi oyenda.
5 Aliyense wopha munthu adzaphedwa, nyama iliyonse yopha munthu
idzaphedwa, munthu aliyense wopha munthu mnzake, adzaphedwa.
6 “Aliyense wopha munthu,
adzaphedwanso ndi munthu;
pakuti Mulungu analenga munthu
m’chifanizo chake.
7 Inu muberekane ndi kuchulukana kuti mudzaze dziko lonse lapansi ndi
kuligonjetsa.”

8 Mulungu anawuza Nowa ndi ana ake kuti, 9 “Tsopano Ine ndapangana
ndi iwe ndi zidzukulu zako zam’tsogolomo, 10 pamodzi ndi zamoyo
zonse, mbalame, ziweto ndi nyama zonse za kuthengo, ndi zonse zimene
zinatuluka m’chombo pamodzi ndi iwe. 11 Pangano langa ndi ili: Ine
ndilonjeza kuti sindidzawononganso zamoyo ndi madzi a chigumula.
Chigumula sichidzawononganso dziko lapansi.”

12 Ndipo Mulungu anati, “Ine ndikupereka chizindikiro ichi cha pangano
langa la pakati pa Ine ndi iwe, ana ako, zamoyo zonse, pamodzi
ndi mibado ya m’tsogolo. 13 Ndayika utawaleza wanga m’mitambo,
ndipo chidzakhala chizindikiro cha pangano langa ndi dziko lapansi.
14 Nthawi zonse pakakhala mitambo mu mlengalenga ndipo utawaleza
uwoneka, 15 ndizikumbukira pangano langa pakati pa Ine ndi inu ndi
zolengedwa zonse. Madzi sadzakhalanso chigumula chowononga dziko
lapansi. 16 Utawaleza ukamadzaoneka m’mitambo, ndidzawuona ndi
kukumbukira pangano losatha pakati pa Mulungu ndi zamoyo zonse pa
dziko lapansi.”

17 Choncho Mulungu anati kwa Nowa, “Ichi ndiye chizindikiro cha
pangano limene ndalichita pakati pa Ine ndi zamoyo zonse pa dziko
lapansi.”

*Ana Aamuna a Nowa*

18 Ana aamuna a Nowa amene anatuluka m'chombo muja anali Semu,
Hamu ndi Yafeti. Hamu anali abambo ake a Kanaani. 19 Ana aamuna a
Nowa amenewa ndiwo anali makolo a anthu onse pa dziko lapansi.

20 Nowa anali munthu woyamba kulima munda wamphesa. 21 Tsiku lina
pamene Nowa anamwako vinyo wa zipatso za m'mundawo analedzera
ndipo anavula zovala zake zonse ndi kugona mu tenti yake ali maliseche.
22 Hamu, abambo ake a Kanaani ataona kuti abambo ake ali maliseche
anakawuza abale ake awiri aja omwe anali panja. 23 Koma Semu ndi
Yafeti anatenga chofunda nachiyika pa mapewa awo; ndipo anayenda
cham'mbuyo naphimba umaliseche wa abambo awo. Anafulatira kuti
asaone umaliseche wa abambo awo.

24 Nowa atadzuka, kuledzera kutatha, ndikudziwa zimene mwana wake
wamng'ono wamwamuna uja anamuchitira, 25 anati,

"Atembereredwe Kanaani!
Adzakhala kapolo
wa pansi kwenikweni kwa abale ake."

26 Anatinso,

"Atamandike Yehova, Mulungu wa Semu!
Kanaani akhale kapolo wa Semu.
27 Mulungu akulitse dziko la Yafeti;
Yafeti alandire madalitso pamodzi ndi Semu,
ndipo Kanaani akhale kapolo wawo."

28 Chitatha chigumula, Nowa anakhala ndi moyo zaka 350.
29 Anamwalira ali ndi zaka 950.

# 10

*Mndandanda wa Mitundu ya Anthu*

1 Nayi mbiri ya ana a Nowa, Semu, Hamu ndi Yafeti. Ana atatuwa
anabereka ana awo chitatha chigumula.

*Banja la Yafeti*

2 Ana aamuna a Yafeti anali:
Gomeri, Magogi, Madai, Yavani, Tubala, Mesaki ndi Tirasi.
3 Ana aamuna a Gomeri anali:
Asikenazi, Rifati ndi Togarima.
4 Ana aamuna a Yavani anali:
Elisa, Tarisisi, Kitimu ndi Rodanimu. 5 (Amenewa ndiwo makolo a
anthu okhala m'mphepete mwa nyanja. Awa ndi ana a Yafeti monga
mwa mafuko a mu mitundu yawo, uliwonse ndi chiyankhulo chake).

*Banja la Hamu*

6 Ana aamuna a Hamu anali:
Kusi, Miziraimu, Puti ndi Kanaani.
7 Ana aamuna a Kusi anali:
Seba, Havila, Sabita, Raama ndi Sabiteka.
Ana aamuna a Raama anali:
Seba ndi Dedani.

8 Kusi anabereka Nimurodi amene anali wankhondo wamphamvu
kwambiri pa dziko lapansi. 9 Iye anali mlenje wamphamvu kwambiri pa-
maso pa Yehova; n'chifukwa chake anthu ali ndi chisudzo, chakuti, "Ndiwe
mlenje wamphamvu kwambiri pamaso pa Yehova monga Nimurodi."

10 Malo oyambirira a ufumu wake anali Babeli, Ereki, Akadi ndi Kaline.
Malo onsewa anali m'dziko la Sinara. 11 Atachoka m'dziko limeneli
anapita ku Asiriya kumene anakamanga Ninive, Rehoboti-Iri, Kala, 12 ndi
Reseni, mzinda waukulu umene uli pakati pa Ninive ndi Kala.

13 Igupto ndiye kholo la
Aludi, Aanami, Alehabu, Anafutu, 14 Apaturusi, Akasilu ndi Akafitori
(kumene kunachokera Afilisti).
15 Kanaani anabereka mwana wake wachisamba,
Sidoni, ndipo anaberekanso Ahiti; 16 Ayebusi, Aamori, Agirigasi;
17 Ahivi, Aariki, Asini, 18 Aaravadi, Azemari ndi Ahamati.

Pambuyo pake, mafuko a Akanaani anafalikira ponseponse, 19 mpaka ku
malire a Kanaani. Malirewo anachokera ku Sidoni kulowa cha ku Gerari
mpaka ku Gaza, ndi kulowa ku Sodomu, Gomora, Adima ndi Zeboimu
mpaka ku Lasa.
20 Amenewa ndiwo ana aamuna a Hamu monga mwa mafuko ndi
ziyankhulo zawo, m'madera omwe amakhala ndi mitundu yawo.

### *Banja la Semu*

21 Semu amene anali mkulu wake wa Yafeti nayenso anabereka nakhala
kholo la Eberi.

22 Ana aamuna a Semu anali:
Elamu, Asuri, Aripakisadi, Ludi ndi Aramu.
23 Ana aamuna a Aramu anali:
Uzi, Huri, Geteri ndi Mesaki.
24 Aripakisadi anabereka Sela,
ndipo Selayo anabereka Eberi.
25 A Eberi anabereka ana aamuna awiri:
Wina anamutcha Pelegi chifukwa pa nthawiyo anthu a pa dziko
lapansi anagawikana. Dzina la m'bale wake linali Yokitani.
26 Yokitani anabereka
Alimodadi, Selefi, Hazari-Maveti, Yera, 27 Hadoramu, Uzali, Dikila,
28 Obali, Abimaeli, Seba, 29 Ofiri, Havila ndi Yobabu. Onsewa anali
ana aamuna a Yokitani.

30 Chigawo chimene ankakhala chinayambira ku Mesa mpaka ku Seferi,
ku dera la mapiri chakummawa.
31 Amenewa ndiwo ana a Semu monga mwa mafuko ndi ziyankhulo
zawo, m'madera omwe ankakhala ndi mitundu yawo.

32 Amenewa ndiwo mafuko a ana aamuna a Nowa monga mwa mibado
ya mitundu yawo. Mitundu yonse ya anthu inatuluka mwa iwowa ndi
kufalikira pa dziko lonse lapansi chitatha chigumula chija.

## 11

### *Nsanja ya Babeli*

1 Nthawi imeneyo anthu onse a pa dziko lapansi ankayankhula
chiyankhulo chimodzi ndipo mawu amene ankayankhula anali amodzi.
2 Pamene anthu amapita chakummawa anapeza chigwa ku dziko la Sinara
nakhazikikako.

3 Tsono anawuzana kuti, “Tiyeni tiwumbe njerwa ndi kuziwotcha
bwinobwino.” Tsono m’malo mwa miyala anagwiritsa ntchito njerwa
zowotcha, ndipo m’malo mwa matope anagwiritsa ntchito phula. 4 Kenaka
anati, “Tiyeni tidzimangire mzinda wokhala ndi nsanja yoti ikafike
kumwamba kuti titchuke. Kupanda kutero tibalalikana pa dziko lonse
lapansi.”
5 Koma Yehova anatsika kudzaona mzindawo ndi nsanja imene anthu
aja ankayimanga. 6 Yehova anati, “Anthuwa ndi amodzi, ndipo ali ndi
chiyankhulo chimodzi. Izi akuchitazi n’chiyambi chabe cha zomwe aku-
funa kukwaniritsa kuchita. 7 Tiyeni titsikireko tikasokoneze chiyankhulo
chawo kuti asamamvetsetsane.”
8 Choncho Yehova anabalalitsa anthu aja pa dziko lonse lapansi ndipo
analeka kumanga mzindawo. 9 N’chifukwa chake mzindawo unatchedwa
Babeli, popeza Yehova anasokoneza chiyankhulo cha anthu onse. Powa-
chotsa kumeneko, Yehova anawabalalitsira pa dziko lonse lapansi.

### *Mibado Kuyambira pa Semu Mpaka Abramu*

10 Nayi mibado yochokera kwa Semu.

Patapita zaka ziwiri chitatha chigumula, Semu ali ndi zaka 100,
anabereka Aripakisadi. 11 Atabereka Aripakisadi, Semu anakhala ndi
moyo zaka 500 ndipo anali ndi ana ena aamuna ndi aakazi.
12 Pamene Aripakisadi anali ndi zaka 35, anabereka Sela. 13 Atabereka
Sela, Aripakisadi anakhala ndi moyo zaka zina 403 ndipo anali ndi ana
ena aamuna ndi aakazi.
14 Pamene Sela anali ndi zaka makumi atatu, anabereka Eberi.
15 Atabereka Eberi, Sela anakhala ndi moyo zaka zina 403 ndipo anali ndi
ana ena aamuna ndi aakazi.
16 Pamene Eberi anali ndi zaka 34 anabereka Pelegi. 17 Atabereka Pelegi,
Eberi anakhala ndi moyo zaka zina 430 ndipo anali ndi ana ena aamuna
ndi aakazi.
18 Pamene Pelegi anali ndi zaka makumi atatu, anabereka Reu.
19 Atabereka Reu, Pelegi anakhala zaka zina 209 ndipo anali ndi ana ena
aamuna ndi aakazi.
20 Pamene Reu anali ndi zaka 32, anabereka Serugi. 21 Atabereka Serugi,
Reu anakhala ndi moyo zaka zina 207 ndipo anali ndi ana ena aamuna ndi
aakazi.
22 Pamene Serugi anali ndi zaka makumi atatu, anabereka Nahori.
23 Atabereka Nahori, Serugi anakhala ndi moyo zaka zina 200 ndipo anali
ndi ana ena aamuna ndi aakazi.
24 Pamene Nahori anali ndi zaka 29, anabereka Tera. 25 Atabereka Tera,
Nahori anakhala ndi moyo zaka zina 119 ndipo anali ndi ana ena aamuna
ndi aakazi.
26 Pamene Tera anali ndi zaka 70, anabereka Abramu, Nahori ndi Harani.

### *Mibado Yochokera mwa Tera*

27 Nayi mibado yochokera mwa Tera.

Tera anabereka Abramu, Nahori ndi Harani. Ndipo Harani anabereka
Loti. 28 Abambo ake a Tera akanali ndi moyo, Harani anamwalira ku
Uri wa ku Akaldeya kumene anabadwira. 29 Abramu ndi Nahori onse
anakwatira. Dzina la mkazi wa Abramu linali Sarai, ndipo la mkazi wa

Nahori linali Milika. Iyeyu ndi Isika abambo awo anali Harani. 30 Sarai
analibe ana chifukwa anali wosabereka.
31 Tera anatenga mwana wake Abramu, mdzukulu wake Loti, ndi
mpongozi wake Sarai, mkazi wa Abramu natuluka mzinda wa Uri wa ku
Akaldeya kupita ku Kanaani. Pamene anafika ku Harani, anakhazikika
kumeneko.
32 Tera anamwalira ku Harani ali ndi zaka 205.

# 12

*Mulungu Ayitana Abramu*

1 Tsiku lina Yehova anamuwuza Abramu kuti, "Tuluka m'dziko lako.
Siya abale ako ndi banja la abambo ako ndipo pita ku dziko limene
ndidzakusonyeza.

2 "Ndidzakusandutsa kholo la mtundu waukulu wa anthu
ndipo ndidzakudalitsa;
ndi kukusandutsa wotchuka kotero kuti
udzakhala dalitso kwa anthu ambiri.
3 Ndidzadalitsa amene adzadalitsa iwe,
ndi kutemberera amene adzatemberera iwe;
ndipo mafuko onse a pa dziko lapansi
adzadalitsika kudzera mwa iwe."

4 Choncho Abramu ananyamuka monga momwe Yehova anamuwuzira,
napita pamodzi ndi Loti. Pamene Abramu amachoka ku Harani n'kuti
ali ndi zaka 75. 5 Abramu anatenga mkazi wake Sarai, Loti, mwana
wamng'ono wake, pamodzi ndi chuma chawo chimene anapeza ndi
antchito amene anali nawo ku Harani. Iwo ananyamuka ulendo mpaka
kukafika ku dziko la Kanaani.
6 Abramu anadutsa m'dzikomo mpaka kukafika ku Sekemu pa mtengo
wa thundu wa ku More. Nthawi imeneyo Akanaani analipobe m'dzikomo.
7 Yehova anadza kwa Abramu nati, "Kwa zidzukulu zako ndidzapereka
dziko limeneli." Choncho Abramu anamangira Yehova amene anadza kwa
iye, guwa lansembe.
8 Atachoka pamenepo analowera cha ku mapiri a kummawa kwa Beteli
namangako tenti yake pakati pa Beteli chakumadzulo ndi Ai chakum-
mawa. Kumeneko anamangira Yehova guwa lansembe napemphera
m'dzina la Yehovayo. 9 Kenaka Abramu ananyamuka kumalowera cha
ku Negevi.

*Abramu ku Igupto*

10 Kunagwa njala yayikulu m'dzikomo, ndipo Abramu anapita ku Igupto
kukakhala ngati mlendo kwa kanthawi kochepa popeza njalayo inakula
kwambiri. 11 Atatsala pang'ono kulowa mu Igupto, Abramu anamuwuza
mkazi wake Sarai kuti, "Ndimadziwa kuti ndiwe mkazi wokongola
kwambiri. 12 Tsono Aigupto akakuona adzanena kuti 'Ameneyu ndi
mkazi wake.' Tsono adzandipha ine nakusiya iwe ndi moyo. 13 Tsono
udzikawawuza kuti iwe ndiwe mlongo wanga. Ukatero zidzandiyendera
bwino ndipo ndidzapulumuka chifukwa cha iwe."
14 Pamene Abramu anafika ku Igupto, Aigupto aja anaona kuti Sarai
anali mkazi wokongoladi. 15 Pamene akuluakulu a ku nyumba ya
Farao anamuona, anakamuyamikira pamaso pa Farao ndipo ananka naye
ku nyumba ya Farao. 16 Abramu naye zinthu zinkamuyendera bwino

chifukwa cha Sarai. Farao anamupatsa nkhosa, ng'ombe, abulu aamuna
ndi abulu aakazi, antchito aakazi pamodzi ndi ngamira.

17 Koma Yehova anabweretsa matenda owopsa pa Farao pamodzi ndi
banja lake lonse chifukwa cha Sarai mkazi wa Abramu. 18 Choncho
Farao anayitanitsa Abramu namufunsa kuti, "N'chiyani wandichitirachi?
N'chifukwa chiyani sunandiwuze kuti ameneyu ndi mkazi wako?
19 N'chifukwa chiyani unati ndi mlongo wako, mpaka ine ndinamutenga
kukhala mkazi wanga? Eko mkazi wako. Mutenge uzipita!" 20 Farao
analamula asilikali ake ndipo iwo anamutulutsa Abramu pamodzi ndi
mkazi wake ndi zonse anali nazo.

# 13

*Abramu Asiyana ndi Loti*

1 Choncho Abramu pamodzi ndi mkazi wake ndi zonse anali nazo,
anachoka ku Igupto kupita ku Negevi. Loti naye anapita nawo. 2 Abramu
anali wolemera kwambiri; anali ndi ziweto ndiponso siliva ndi golide.

3 Atachoka ku Negevi, anayenda malo osiyanasiyana mpaka anafika
ku Beteli, ku malo a pakati pa Beteli ndi Ai, kuja kumene anamanga
tenti poyamba, 4 ndiponso kumene Abramu anamangira Yehova guwa
lansembe kwa nthawi yoyamba ndi kupemphera m'dzina la Yehova.

5 Loti amene ankayendayenda ndi Abramu nayenso anali ndi ziweto
zosiyanasiyana ndi matenti. 6 Motero dziko linayamba kuwachepera
kuti onse n'kukhala pamodzi, popeza katundu wawo anali wochuluka
kwambiri moti sakanatha kukhala pamodzi. 7 Mikangano inayambika
pakati pa abusa a Abramu ndi abusa a Loti. Nthawi imeneyo n'kuti
Akanaani ndi Aperezi akukhalanso m'dziko lomwelo.

8 Tsono Abramu anati kwa Loti, "Pasakhale mikangano pakati pa iwe
ndi ine kapena pakati pa abusa ako ndi anga, popeza ndife abale. 9 Kodi
dziko lonseli silili pamaso pako? Tiye tisiyane. Iwe ukalowera kumanzere,
ine ndilowera kumanja; ukalowera kumanja, ine ndipita kumanzere."

10 Loti atamwazamwaza maso anaona kuti chigwa chonse cha mtsinje
wa Yorodani chinali chothiriridwa bwino ngati munda wa Yehova, kapena
ngati dziko la ku Igupto mpaka ku Zowari. (Nthawi iyi n'kuti Yehova
asanawononge Sodomu ndi Gomora). 11 Choncho Loti anadzisankhira
yekha chigwa chonse cha Yorodani nanyamuka kulowera cha kummawa.
Choncho anthu awiriwa anasiyana. 12 Abramu anakhala m'dziko la
Kanaani, pamene Loti anakakhala pakati pa mizinda ikuluikulu ya
m'chigwamo. Anamanga tenti yake pafupi ndi Sodomu. 13 Tsono anthu a
ku Sodomu anali oyipa ndiponso ankachimwira Yehova kwambiri.

14 Loti atachoka, Yehova anati kwa Abramu, "Kuchokera pamene ulipo
tayang'anayang'ana cha kumpoto, kummwera, kummawa ndi kumadzulo.
15 Dziko lonse ukulionalo ndidzalipereka kwa iwe ndi zidzukulu zako
mpaka muyaya. 16 Ndidzakupatsa zidzukulu zochuluka ngati fumbi
lapansi moti amene angathe kuwerenga fumbilo ndiye kuti angathenso
kuwerenga zidzukulu zako. 17 Dzuka ndipo uyendere dziko lonseli mulitali
ndi mulifupi pakuti ndalipereka kwa iwe."

18 Choncho Abramu anasamutsa tenti yake napita kukakhala pafupi
ndi mitengo ikuluikulu ija ya thundu ya ku Mamre ku Hebroni, kumene
anamangira Yehova guwa lansembe.

# 14

*Abramu Apulumutsa Loti*

1 Pa nthawi imeneyi Amarafeli mfumu ya Sinara, Arioki mfumu ya
Elasara, Kedorilaomere mfumu ya Elamu ndi Tidala mfumu ya Goimu
2 anathira nkhondo Bera mfumu ya ku Sodomu, Birisa mfumu ya Gomora,
Sinabi mfumu ya Adima, Semeberi mfumu ya Ziboimu ndi mfumu ya
Bela (kumeneko ndi ku Zowari). 3 Mafumu onse anathiridwa nkhondowa
anagwirizana pamodzi kupita ku Chigwa cha Sidimu (Nyanja ya Mchere).
4 Kwa zaka khumi ndi ziwiri anali pansi pa ulamuliro wa Kedorilaomere,
koma m'chaka cha khumi ndi chitatu anamuwukira.

5 M'chaka cha khumi ndi chinayi, Kedorilaomere mogwirizana ndi
mafumu ena aja anapita kukagonjetsa Arefaiwa ku Asiteroti-karanaimu,
Zuzimu wa ku Hamu, Aemi wa ku Savekiriataimu 6 amene ankakhala
ku Ahori, ku dziko la mapiri la Seiri mpaka ku Eli Parani kufupi ndi
chipululu. 7 Kenaka anabwerera napita ku Eni-Misipati (ku Kadesi),
ndipo anagonjetsa dera lonse la Aamaleki, kuphatikizanso Aamori amene
ankakhala ku Hazazoni Tamara.

8 Tsono mafumu a ku Sodomu, Gomora, Adima, Zeboimu ndi ku
Bela (ku Zowari) anapita ku Chigwa cha Sidimu kukakonzekera kuthira
nkhondo 9 Kedorilaomere mfumu ya Elamu, Tidala mfumu ya Goimu,
Amarafeli mfumu ya Sinara ndi Arioki mfumu ya Elasara. Mafumu anayi
analimbana ndi mafumu asanu. 10 Koma Chigwa cha Sidimu chinali
chodzaza ndi maenje aphula. Choncho pamene mafumu a ku Sodomu
ndi Gomora amathawa, ankhondo ena anagweramo ndipo ena anathawira
ku mapiri. 11 Mafumu anayi aja anatenga katundu yense ndi chakudya
chonse cha ku Sodomu ndi Gomora napita nazo. 12 Anatenganso Loti,
mwana wa m'bale wake wa Abramu pamodzi ndi katundu wake popeza
ankakhala mu Sodomu.

13 Koma munthu wina amene anathawa, anabwera kudzamufotokozera
Abramu Mhebri. Tsono Abramu ankakhala pafupi ndi mitengo ikuluikulu
ya thundu ya Mamre wa fuko la Aamori, m'bale wake wa Esikolo ndi
Aneri. Onsewa anali pa mgwirizano ndi Abramu. 14 Abramu atamva
kuti Loti wagwidwa pa nkhondo, anasonkhanitsa asilikali 318 obadwira
m'banja lake lomwelo nalondola mpaka ku Dani. 15 Pa nthawi ya usiku
Abramu anawagawa asilikali ake kuti athire nkhondo mafumu aja, ndipo
anawakantha nawapirikitsa mpaka ku Hoba, cha kumpoto kwa Damasiko.
16 Ndipo anawalanda katundu wawo yense nabwera naye Loti, katundu
wake yense, pamodzi ndi akazi ndi anthu ena.

17 Abramu atabwerera kuchokera kogonjetsa Kedorilaomere ndi ma-
fumu amene anali nawo pa mgwirizano, mfumu ya ku Sodomu inabwera
kudzakumana naye ku Chigwa cha Save (chimenechi ndicho Chigwa cha
Mfumu).

18 Ndipo Melikizedeki mfumu ya ku Salemu anabweretsa buledi ndi
vinyo. Iyeyu anali wansembe wa Mulungu Wammwambamwamba,
19 ndipo anadalitsa Abramu nati,

"Mulungu Wammwambamwamba,
wolenga kumwamba ndi dziko lapansi, akudalitse iwe Abramu.
20 Ndipo adalitsike Mulungu Wammwambamwamba
amene anapereka adani ako m'dzanja lako."

Ndipo Abramu anamupatsa iye chakhumi cha zonse anali nazo.

21 Mfumu ya Sodomu inati kwa Abramu, “Ine undipatse anthu okhawo,
koma katundu akhale wako.”
22 Koma Abramu anawuza mfumu ya Sodomu kuti, “Ndakweza
manja anga kwa Yehova, Mulungu Wammwambamwamba, Mlengi
wakumwamba ndi dziko lapansi, kulumbira 23 kuti sindidzalandira
kanthu kalikonse kako, ngakhale utakhala ulusi chabe kapena chingwe
cha nsapato, kuopa kuti ungamanene kuti, ‘Ndamulemeretsa Abramu.’
24 Sindidzalandira kanthu kalikonse kupatula zokhazo zimene anthu anga
adya ndi gawo la katundu la anthu amene ndinapita nawo monga Aneri,
Esikolo ndi Mamre. Iwowa atenge gawo lawo.”

# 15

*Pangano la Mulungu ndi Abramu*

1 Zitatha izi, Yehova anayankhula ndi Abramu m’masomphenya nati:
“Usaope Abramu.
Ine ndili ngati chishango chokutchinjiriza.
Mphotho yako idzakhala yayikulu.”
2 Koma Abramu anati, “Haa! Ambuye Yehova, mukhoza kundipatsa
chiyani popeza ndikanali wopanda mwana ndipo amene adzatenge chuma
changa ndi Eliezara wa ku Damasiko? 3 Inu simunandipatse ana kotero
kuti wantchito wa ku nyumba kwanga ndiye amene adzalowe m’malo
mwanga.”
4 Yehova anayankhula naye nati: “Munthu uyu sadzalowa m’malo
mwako, koma mwana wako weniweni wamwamuna, wobereka wekha
ndiye adzalowe m’malo mwako.” 5 Yehova anapita naye Abramu
panja nati, “Tayang’ana kumwambaku, ndipo chifukwa cha chimenechi
uwerenge nyenyezi ngati ungathe kuziwerenga.” Ndipo anamuwuza kuti,
“Ndi mmene adzakhalire ana ako ndi zidzukulu zako.”
6 Abramu anakhulupirira Yehova, ndipo ichi chinamuchititsa kukhala
wolungama.
7 Ndipo anamuwuza kuti, “Ine ndine Yehova amene ndinakuchotsa iwe
ku mzinda wa Uri wa ku Akaldeya kuti ndikupatse dziko ili kuti likhale
lako.”
8 Koma Abramu anati, “Haa! Ambuye Yehova, kodi ndingadziwe bwanji
kuti lidzakhaladi langa?”
9 Kotero Yehova anati kwa iye, “Kanditengere kamsoti kang’ombe ka
zaka zitatu, kamsoti ka mbuzi ka zaka zitatu, ndi nkhosa yayimuna ya
zaka zitatu pamodzi ndi nkhunda ndi kamwana ka njiwa.”
10 Abramu anabweretsadi zonsezi nadula chilichonse pakati
n’kuzindandalika, chidutswa chilichonse kuyang’anana ndi chinzake;
koma njiwa ndi nkhunda sanazidule pakati. 11 Pamene miphamba
inabwera kuti itole nyama ija, Abramu anayipirikitsa.
12 Pamene dzuwa limalowa Abramu anagona tulo tofa nato ndipo
mdima wandiweyani ndi wochititsa mantha unamuphimba. 13 Tsono
Yehova anati kwa iye, “Uyenera kudziwa mosakayika kuti zidzukulu
zako zidzakhala alendo m’dziko lachilendo ndipo zidzakhala akapolo ndi
kuzunzidwa zaka 400. 14 Koma ndidzalanga dziko limene zidzukulu zako
zidzagwireko ukapolo ndipo pambuyo pake iwo adzatulukamo ndi chuma
chambiri. 15 Komabe iweyo udzamwalira mu mtendere ndi kuyikidwa
m’manda utakalamba bwino. 16 Patapita mibado inayi, adzukulu ako
adzabwereranso kuno popeza tchimo la Aamori silinafike pachimake kuti
alangidwe.”

17 Dzuwa litalowa ndipo mdima utagwa, panaoneka m'phika wofuka
nthunzi ya moto ndi sakali yoyaka ndipo zinadutsa pakati pa zidutswa
za nyama zija. 18 Pa tsiku limenelo, Yehova anachita pangano ndi
Abramu nati, "Ndikulonjeza kuti ndidzapereka dziko ili kwa zidzukulu
zako, kuchokera ku mtsinje wa ku Igupto mpaka ku mtsinje waukulu wa
Yufurate. 19 Ndidzakupatsani dziko la Akeni, Akenizi, Akadimoni, 20 Ahiti,
Aperezi, Arefaimu, 21 Aamori, Akanaani, Agirigasi ndi Ayebusi."

# 16

*Sarai ndi Hagara*

1 Tsono Sarai, mkazi wa Abramu anali asanamuberekere ana Abramuyo.
Koma anali ndi wantchito wamkazi wa ku Igupto dzina lake Hagara;
2 ndipo Sarai anati kwa Abramu, "Yehova sanalole kuti ine ndikhale ndi
ana. Bwanji mulowe mwa wantchito wanga wamkaziyu kuti mwina
ndingaone ana kudzera mwa iyeyu."

Abramu anamvera Sarai. 3 Tsono Sarai anatenga Hagara wantchito wake
wamkazi wa ku Igupto uja namupereka kwa Abramu mwamuna wake kuti
akhale mkazi wake. Izi zinachitika Abramu atakhala ku Kanaani zaka
khumi. 4 Abramu atalowana ndi Hagara, Hagara uja anatenga mimba.

Pamene Hagara anadziwa kuti anali woyembekezera anayamba kun-
yoza mbuye wake Sarai. 5 Pamenepo Sarai anati kwa Abramu, "Inu
ndinu amene mwandiputira nkhanza zikundichitikirazi. Ndinakupatsani
wantchito wanga wamkazi kuti akhale mkazi wanu, ndiye tsopano
wayamba kundinyoza ine chifukwa wadziwa kuti ndi woyembekezera.
Yehova ndiye amene aweruze pakati pa inu ndi ine."

6 Abramu anati, "Wantchito wakoyu ali m'manja mwako. Chita naye
chilichonse chimene ukuganiza kuti ndi chokukomera." Tsono Sarai
anazunza Hagara mpaka anathawa.

7 Mngelo wa Yehova anamupeza Hagara pafupi ndi chitsime
m'chipululu. Chinali chitsime chimene chili m'mphepete mwa msewu
wopita ku Suri. 8 Ndipo mngeloyo anati, "Hagara, iwe wantchito wa Sarai,
ukuchokera kuti ndipo ukupita kuti?"

Iye anayankha, "Ndikuthawa mbuye wanga Sarai."

9 Mngelo wa Yehova anamuwuza kuti, "Bwerera kwa mbuye wako
ndipo ukamugonjere. 10 Ndidzakupatsa zidzukulu zambiri zoti munthu
sangaziwerenge."

11 Mngelo wa Yehova uja anamuwuzanso kuti,

"Ndiwe woyembekezera
ndipo udzabala mwana wamwamuna.
Udzamutcha dzina lake Ismaeli,
pakuti Yehova wamva kulira chifukwa cha kuzunzika kwako.
12 Iye adzakhala munthu wa khalidwe ngati m'mbulu wamisala;
adzadana ndi aliyense
ndipo anthu onse adzadana naye,
adzakhala mwaudani pakati pa abale ake
onse."

13 Hagara anatcha Yehova amene anamuyankhula uja dzina loti: "Ndinu
Mulungu amene mumandiona," popeza anati, "Ndakumana ndi Yehova
atatha kundikomera mtima." 14 N'chifukwa chake chitsime chija chimene
chili pakati pa Kadesi ndi Beredi chinatchedwa Beeri-lahai-roi.

15 Tsono Hagara anamuberekera Abramu mwana wamwamuna ndipo
Abramu anamutcha mwanayo Ismaeli. 16 Pamene Hagara anamubalira
Ismaeli n'kuti Abramuyo ali ndi zaka 86.

## 17

*Pangano la Mdulidwe*

1 Pamene Abramu anali ndi zaka 99, Yehova anamuonekera nati, "Ine
ndine Mulungu Wamphamvuzonse. Ukhale munthu wochita zolungama
nthawi zonse. 2 Ndipo Ine ndikulonjeza kuti ndidzakupatsa zidzukulu
zambiri."
3 Pomwepo Abramu anadziponya pansi ndipo Mulungu anati kwa iye,
4 "Pangano langa ndi iwe ndi ili: Udzakhala kholo la mitundu yambiri
ya anthu. 5 Sudzatchedwanso Abramu; dzina lako lidzakhala Abrahamu,
chifukwa ndakusandutsa kukhala kholo la mitundu yambiri ya anthu.
6 Ndidzakupatsa zidzukulu zambiri motero kuti mitundu yambiri ya anthu
idzatuluka mwa iwe. Mafumunso adzatuluka mwa iwe. 7 Pangano langa
ndi iwe pamodzi ndi zidzukulu za mibado ya m'tsogolo lidzakhala la
muyaya. Ndidzakhala Mulungu wako ndi Mulungu wa zidzukulu zako.
8 Dziko lonse la Kanaani, limene iwe ukukhala tsopano, ndalipereka kwa
iwe ndi kwa zidzukulu zako kuti likhale chuma chanu mpaka muyaya.
Ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wa zidzukulu zako."
9 Kenaka Mulungu anati kwa Abrahamu, "Koma iwe pamodzi ndi
zidzukulu zako zobwera pambuyo pako m'mibado ya m'tsogolomo, sun-
gani pangano langali. 10 Iwe pamodzi ndi zidzukulu zako zobwera pam-
buyo pako muzisunga pangano ili loti mwamuna aliyense pakati panupa
azichita mdulidwe. 11 Kuyambira tsopano muzichita mdulidwe ndipo
ichi chidzakhala chizindikiro cha pangano langa ndi iwe. 12 Kuyambira
tsopano mpaka mibado ya m'tsogolomo mwana wamwamuna aliyense
pakati panu amene wakwana masiku asanu ndi atatu ayenera kuchita
mdulidwe. Awa ndi ana obadwa m'banja lako, kapena akapolo ochita
kugula ndi ndalama, mlendo osakhala wa m'mbumba yako. 13 Achite
mdulidwe ndithu mwana wamwamuna aliyense, mbadwa ngakhale
kapolo wochita kugula ndi ndalama, ndipo ichi chidzakhala chizindikiro
pa thupi lanu cha pangano langa lamuyaya. 14 Mwamuna aliyense
amene adzakhala wosachita mdulidwe adzachotsedwa pakati pa anthu
ake chifukwa sanasunge pangano langa."
15 Mulungu anatinso kwa Abrahamu, "Sarai mkazi wako, sudza-
mutchanso Sarai; dzina lake lidzakhala Sara. 16 Ndidzamudalitsa ndipo
adzakubalira mwana wamwamuna. Ndidzamudalitsa kuti akhale mayi
wa mitundu ya anthu; mafumu a anthuwo adzachokera mwa iye."
17 Abrahamu anadzigwetsa pansi pamaso pa Yehova, Iye anaseka nati,
"Kodi munthu wa zaka 100 n'kubala mwana? Kodi Sara adzabereka
mwana pa msinkhu wa zaka makumi asanu ndi anayi?" 18 Ndipo
Abrahamu anati kwa Mulungu, "Bwanji mumudalitse Ismaeli."
19 Koma Mulungu anati, "Ayi, koma mkazi wako Sara adzakubalira
mwana wamwamuna, ndipo udzamutcha Isake. Ndidzasunga pangano
langa losatha ndi iyeyu komanso ndi zidzukulu zobwera pambuyo pake.
20 Koma za Ismaeli, ndamva. Ndidzamudalitsadi, ndipo adzakhala ndi
zidzukulu zambiri. Iye adzakhala kholo la mafumu khumi ndi awiri ndipo
mwa iye mudzatuluka mtundu waukulu wa anthu. 21 Koma ndidzasunga
pangano langali ndi Isake amene Sara adzakubalira pofika nthawi ngati

ino chaka chamawa.” 22 Atatha kuyankhula, Mulungu anamuchokera
Abrahamu.
23 Tsono Abrahamu anachita mdulidwe mwana wake Ismaeli ndi onse
amene anali m’banja lake, mbadwa ngakhale kapolo ochita kugula ndi
ndalama, monga mmene Mulungu analamulira. 24 Abrahamu anali ndi
zaka 99 pamene anachita mdulidwe, 25 ndipo mwana wake Ismaeli anali
ndi zaka khumi ndi zitatu; 26 Onse, Abrahamu ndi mwana wake Ismaeli,
anachita mdulidwe tsiku limodzi. 27 Aliyense wamwamuna wa pa banja
pa Abrahamu, kuphatikizapo iwo amene anabadwira pa banja pomwepo
kapena akapolo ogula ndi ndalama kwa alendo, anachita mdulidwe.

# 18

### *Alendo Atatu a Abrahamu*

1 Yehova anadza kwa Abrahamu pafupi ndi mitengo ikuluikulu ya
thundu ya ku Mamre. Abrahamu n’kuti atakhala pansi pa khoma la
tenti yake masana, dzuwa likutentha. 2 Tsono Abrahamu atakweza
maso ake patali anangoona anthu atatu atayima cha potero. Atawaona,
ananyamuka mofulumira kuti awachingamire. Atafika anaweramitsa
mutu pansi mwa ulemu nati, 3 “Ngati mwandikomera mtima, mbuye
wanga, musamulambalale mtumiki wanu. 4 Ndikupatseniko timadzi
pang’ono kuti nonse musambitse mapazi anu ndi kupumula pansi pa
mtengo uwu. 5 Tsono ndikutengereniko kachakudya kuti mudye kuti
mwina n’kupezako mphamvu zopitirizira ulendo wanu. Inu mwafika
kumalo kwa mtumiki wanu.”

Ndipo iwo anamuyankha nati, “Zikomo kwambiri, chita monga wanenera.”

6 Choncho Abrahamu anafulumira kupita kwa Sara m’tenti nati, “Tafulumira, tenga mabeseni atatu a ufa wosalala, ukande ndi kupanga buledi.”

7 Kenaka Abrahamu anakatenga mwana wang’ombe wonenepa ndi
wofewa bwino ndi kupatsa wantchito wake amene anachita changu
kukonza ndiwoyo. 8 Tsono Abrahamu anatenga chambiko, mkaka ndi
mwana wang’ombe wokonzedwa uja nazipereka kwa anthu aja. Alendowo akudya, Abrahamu ankawayang’ana atayimirira pansi pa mtengo.

9 Anthuwo anafunsa Abrahamu kuti, “Mkazi wako Sara ali kuti?”

Iye anati, “Ali mu tentimu.”

10 Tsono mmodzi mwa iwo anati, “Mosakayikira ndidzabweranso pa nthawi ngati yomwe ino chaka chamawa, ndipo Sara mkazi wako adzakhala ndi mwana wamwamuna.”

Koma Sara amene anali kumbuyo kwa Abrahamu pa khoma la tenti
ankamva zonsezi. 11 Abrahamu ndi Sara anali okalamba kale ndipo
anali ndi zaka zambiri. Sara n’kuti atapyola kale pa msinkhu oti
n’kubereka. 12 Choncho anangoseka nati mu mtima mwake, “Kodi munthu
wothayitha ngati ine ndingasangalalenso kugona pamodzi ndi mbuye
wanga? Mwamuna wanga nayenso ndi wokalamba.”

13 Ndipo Yehova anati kwa Abrahamu, “N’chifukwa chiyani Sara
anaseka n’kumati, ‘Moti ine n’kudzakhaladi ndi mwana mmene
ndakalambiramu?’ 14 Kodi pali chimene chikhoza kumukanika Yehova?
Pa nthawi yake, ngati yomwe ino chaka chamawa ndidzabweranso, ndipo
Sara adzabala mwana wamwamuna.”

15 Koma Sara ndi mantha ananama nati, “Sindinaseke.”

Koma Iye anati, “Inde iwe unaseka.”

*Abrahamu Apembedzera Sodomu*

16 Kenaka anthu aja ananyamuka ndi kumapita, molunjika ku Sodomu.
Ndipo Abrahamu anayenda nawo pamodzi kuwaperekeza. 17 Tsono
Yehova anati mu mtima mwake, “Kodi ndingamubisire Abrahamu
chimene ndikuti ndichite posachedwa? 18 Abrahamu adzakhaladi mtundu
wa anthu waukulu ndi wamphamvu, ndipo mitundu yonse ya anthu pa
dziko lapansi adzadalitsika kudzera mwa iye. 19 Pakuti ndasankha iyeyu
kuti adzatsogolere ana ake ndi a pa banja lake, kuti asunge mawu a
Yehova pochita zoyenera ndi zachilungamo. Choncho Yehova adzachita
kwa Abrahamu chimene anamulonjeza iye.”

20 Ndipo Yehova anati kwa Abrahamu, “Kulirira Gomora kwakula
ndipo tchimo lawo lafika poyipa kwambiri 21 choncho ndikuti ndipiteko
ndikaone ngati zimene achita zilidi zoyipa monga mmene madandawulo
andipezera Ine. Ngati sizili choncho, ndikadziwa.”

22 Anthu aja anatembenuka n’kumapita, kulowera ku Sodomu, koma
Abrahamu anali chiyimirire pamaso pa Yehova. 23 Kenaka Abrahamu
anasendera kufupi ndi Iye nati, “Kodi mudzawonongera kumodzi wol-
ungama ndi woyipa? 24 Nanga bwanji patakhala anthu makumi asanu
olungama mu mzindamo? Kodi mudzawonongadi onse osausiyako mzin-
dawo chifukwa cha anthu makumi asanu olungama omwe ali m’menemo?
25 Ndithu simungachite zimenezi, kupha anthu olungama pamodzi ndi
oyipa. N’zosatheka kuti inu n’kufananitsa olungama ndi oyipa. Kodi
woweruza wa dziko lapansi n’kulephera kuchita chilungamo?”

26 Yehova anati, “Nditapeza anthu makumi asanu olungama mu mzinda
wa Sodomu, ndidzasiya malo onsewo osawawononga chifukwa cha iwo.”

27 Ndipo Abrahamu anayankhulanso nati, “Tsono poti ndalimba mtima
kuyankhula ndi Ambuye, ngakhale kuti ndine fumbi ndi phulusa chabe,
28 bwanji anthu olungama atacheperapo ndi asanu pa anthu makumi
asanu? Kodi mudzawononga mzinda wonse chifukwa cha asanuwo?”

Iye anati, “Nditapezamo anthu 45, sindidzawuwononga.”

29 Kenakanso anayankhula kwa Iye nati, “Bwanji atangopezekamo anthu
40 okha?”

Iye anayankha, “Chifukwa cha anthu 40 amenewa, sindidzatero.”

30 Ndipo Abrahamu anati, “Pepanitu musandipsere mtima Ambuye,
koma mundilole kuti ndiyankhule. Nanga mutapezekamo anthu makumi
atatu okha?”

Iye anayankha, “Sindidzatero ngati atapezekamo anthu makumi atatu.”

31 Abrahamu anati, “Tsono poti ndalimba mtima chonchi kumayankhula
ndi Ambuye, bwanji atangopezeka anthu makumi awiri okha?”

Iye anati, “Chifukwa cha anthu makumi awiriwo, sindidzawuwononga.”

32 Kenaka Abrahamu anati, “Pepani Ambuye musandipsere mtima,
ndingoyankhula kamodzi kokhaka basi. Bwanji atangopezeka khumi okha
m’menemo?”

Iye anayankha nati, “Chifukwa cha khumiwo, sindidzawuwononga.”

33 Yehova atatsiriza kuyankhula ndi Abrahamu, anachoka ndipo Abra-
hamu anabwerera ku nyumba yake.

## 19

*Kuwonongedwa kwa Sodomu ndi Gomora*

1 Angelo awiri aja anafika ku Sodomu madzulo ndipo Loti anali
atakhala pansi pa chipata cha mzindawo. Loti atawaona, anayimirira
ndi kukakumana nawo ndipo anaweramitsa mutu wake pansi mwaulemu.
2 Iye anati, “Ambuye wanga, chonde patukirani ku nyumba kwa mtumiki
wanu. Mukhoza kusambitsa mapazi anu ndi kugona usiku uno kenaka
n’kumapitirira ndi ulendo wanu mmamawa.”

Iwo anati, “Ayi, tigona panja.”

3 Koma iye anawawumiriza kwambiri kotero kuti anapita naye pamodzi
ku nyumba kwake. Anawakonzera chakudya buledi wopanda yisiti ndipo
anadya. 4 Alendo aja asanapite kogona, amuna onse achinyamata ndi
achikulire ochokera mbali zonse za mzinda wa Sodomu anazinga nyumba
ya Loti. 5 Iwo anayitana Loti namufunsa kuti, “Ali kuti amuna aja amene
afika kuno usiku womwe uno? Atulutse, utipatse kuti tigone nawo malo
amodzi.”

6 Loti anatuluka panja kukakumana nawo natseka chitseko 7 ndipo
anati, “Ayi anzanga, musachite zinthu zoyipa zotere. 8 Taonani, ine ndili
ndi ana anga akazi awiri amene sanagonepo ndi mwamuna. Mundilole
ndikutulutsireni amenewo ndipo muchite nawo zimene mungafune.
Koma musachite chilichonse ndi anthuwa, pakuti iwowa ndi alendo anga
ndipo ndiyenera kuwatchinjiriza.”

9 Iwo anayankha kuti, “Tachoka apa tidutse.” Ndipo anati, “Munthu
uyu anabwera kuno ngati mlendo chabe, tsono lero akufuna kuti akhale
wotiweruza! Tikukhawulitsa kuposa iwowa.” Anapitiriza kumuwumiriza
Loti uja n’kumasunthira kutsogolo kuti athyole chitseko.

10 Koma anthu aja anali m’katiwa anasuzumira namukokera Loti uja
m’kati mwa nyumba n’kutseka chitseko. 11 Kenaka anawachititsa khungu
anthu amene anali panja pa nyumba aja, aang’ono ndi aakulu omwe, kuti
asaone pa khomo.

12 Anthu awiri aja anati kwa Loti, “Kodi uli ndi wina aliyense pano,
kaya ndi akamwini ako, kaya ndi ana ako aamuna kapena aakazi,
kapena aliyense mu mzindamu amene ndi anzako? Atulutse onse muno,
13 chifukwa tiwononga malo ano. Yehova waona kuti kuyipa kwa anthu a
mu mzindawu kwakulitsa. Choncho watituma kuti tiwuwononge.”

14 Choncho Loti anatuluka nayankhula ndi akamwini ake amene anali
kuyembekezera kukwatira ana ake akazi nati, “Fulumirani, tiyeni tichoke
pa malo ano chifukwa Yehova watsala pang’ono kuwononga mzindawu.”
Koma akamwini akewo ankayesa kuti akungoselewula.

15 Mmene kumacha, angelo aja anamufulumizitsa Loti nati, “Nyamuka,
tenga mkazi wako ndi ana ako aakazi awiriwo, ndipo mutuluke mu
mzindawo kuopa kuti mungaphedwe pamodzi nawo.”

16 Koma Loti ankakayikabe. Koma Yehova anawachitira chi-
fundo motero kuti anthu aja anagwira mkazi wake ndi ana ake
aakazi aja nawatsogolera bwinobwino kuwatulutsa mu mzindawo.
17 Atangowatulutsa, mmodzi wa angelowo anati, “Thawani kuti mudzip-
ulumutse, musachewuke, musayime pena paliponse m’chigwamo!
Thawirani ku mapiri kuopa kuti mungawonongeke!”

18 Koma Loti anawawuza kuti, “Ayi, ambuye anga chonde musatero!
19 Taonani, Inu mwachitira mtumiki wanu chifundo, ndipo mwaonetsa
kukoma mtima kwanu pondipulumutsa. Sindingathawire ku mapiri
chifukwa chiwonongekochi chikhoza kundipeza ndisanafike ku mapiriko
ndipo ndingafe. 20 Koma, chapafupi pomwepa pali mudzi woti ndikhoza

kuthamanga n'kukafikako. Mundilole ndithawireko, ndi waung'ono
kwambiri, si choncho? Mukatero, moyo wanga upulumuka."
21 Mngeloyo anati kwa iye, "Chabwino, ndavomeranso pempho lako,
sindiwononga mudzi ukunenawo. 22 Koma uthawireko mofulumira
chifukwa sindichita kena kalikonse mpaka utafikako." (N'chifukwa chake
mudziwo unatchedwa Zowari).
23 Pamene Loti amafika ku Zowari, n'kuti dzuwa litatuluka. 24 Ndiye
Yehova anathira sulufule wamoto wochokera kumwamba kwa Yehova pa
Sodomu ndi Gomora. 25 Kotero, anawononga mizindayo, chigwa chonse
pamodzi ndi onse okhala m'mizindayo. Anawononganso zomera zonse za
m'dzikolo. 26 Koma mkazi wa Loti anachewuka ndipo anasanduka mwala
wa mchere.
27 Mmawa mwake, Abrahamu ananyamuka nabwerera kumalo kumene
anakumana ndi Yehova kuja. 28 Anayang'ana kumunsi ku Sodomu,
Gomora ndi ku dziko lonse la ku chigwa, ndipo anaona chiwutsi chikufuka
m'dzikolo ngati chikuchokera m'ng'anjo.
29 Choncho Mulungu anawononga mizinda ya ku chigwa, koma anakum-
bukira pemphero la Abrahamu natulutsa Loti ku sulufule ndi moto zimene
zinawononga mizinda ya kumene Loti amakhalako.

### *Loti ndi Ana ake Aakazi*

30 Loti ndi ana ake awiri aakazi anachoka ku Zowari nakakhala ku
mapiri, chifukwa amachita mantha kukhala ku Zowari. Iye ndi ana ake
awiri ankakhala m'phanga. 31 Tsiku lina mwana wake wamkazi wamkulu
anawuza mng'ono wake kuti, "Abambo athu ndi wokalamba ndipo palibe
mwamuna aliyense pano woti atikwatire ndi kubereka ana monga mwa
chikhalidwe cha pa dziko lonse lapansi. 32 Tiye tiwamwetse vinyo ndipo
tigone nawo. Tikatero mtundu wathu udzakhalapobe."
33 Usiku umenewo analedzeretsa vinyo abambo awo, ndipo wamkuluyo
analowa nagona naye. Abambo awo samadziwa kanthu pamene mwanayo
anagona naye kapena pamene anadzuka.
34 Tsiku linali mwana wamkazi wamkulu uja anati kwa mng'ono wake,
"Usiku wathawu ine ndinagona ndi abambo anga. Tiye tiwaledzeretsenso
vinyo usiku uno ndipo iwe upite ndi kugona nawo ndipo mtundu wathu
udzakhalapobe." 35 Choncho analedzeranso vinyo abambo awo usiku
umenewonso, ndipo mwana wamkazi wamng'ono anapita nagona nawo.
Abambo awo sanadziwenso kanthu pamene mwanayo anagona naye
kapena pamene anadzuka.
36 Choncho ana onse awiri a Loti aja anatenga pathupi pa abambo
awo. 37 Mwana wamkazi wamkulu uja anabereka mwana wa mwamuna
ndipo anamutcha Mowabu. Iyeyo ndiye kholo la Amowabu onse.
38 Mwana wamkazi wamng'ono naye anabereka mwana wamwamuna,
ndipo anamutcha iye Beni-Ammi. Iyeyu ndiye kholo la Aamoni onse.

## 20

### *Abrahamu ndi Mfumu Abimeleki*

1 Abrahamu anachokako kumeneko napita ku Negevi ndipo anakakhala
ku dziko la Gerari, limene lili pakati pa mzinda wa Kadesi ndi mzinda wa
Suri. Anakhala ku Gerari kwa kanthawi, 2 ndipo Abrahamu ankawawuza
za Sara kuti, "Iyeyu ndi mlongo wanga." Choncho Abimeleki, mfumu wa
ku Gerari anamutenga Sara uja.

3 Koma usiku, Mulungu anafika kwa Abimeleki kutulo nati, “Ufatu iwe
chifukwa cha mkazi amene watengayu popeza ndi wokwatiwa.”
4 Nthawi imeneyi n’kuti Abimeleki asanamukhudze mkaziyo, kotero
kuti anati, “Ambuye, kodi mudzawonongadi mtundu wolungama? 5 Kodi
Abrahamu sanandiwuze kuti iyeyu ndi mlongo wake? Ndiponso mkaziyu
ankanena kuti Abrahamu ndi mlongo wake. Choncho ine pochita izi,
ndinkachita moona mtima ndiponso mopanda chinyengo.”
6 Tsono kumaloto komweko Mulungu anati kwa iye, “Inde ndikudziwa
kuti wachita izi moona mtima, ndipo Ine sindinafune kuti undichimwire.
N’chifukwa chake sindinakulole kuti umukhudze. 7 Tsopano kabwezere
mkaziyo kwa mwamuna wake. Iyeyu ndi mneneri, ndipo adzakupempher-
era kuti ukhale ndi moyo. Koma ukapanda kukamupereka, udziwiretu
kuti udzafa pamodzi ndi onse a pa banja pako.”
8 Mmamawa mwake Abimeleki anayitanitsa akuluakulu ake onse, ndipo
atawafotokozera zimene zinachitika, iwo aja anachita mantha kwambiri.
9 Kenaka Abimeleki anayitana Abrahamu ndipo anati, “Kodi wachita
chiyani? Ndakulakwira chiyani kuti undibweretsere ine pamodzi ndi
anthu anga chilango chachikulu chotere? Wandichitira zinthu zimene
sizinayenera kuchitika.” 10 Ndipo Abrahamu anafunsa Abimeleki kuti,
“Chifukwa chiyani wachita zimenezi?”
11 Abrahamu anayankha nati, “Ndinkaganiza kuti kuno kulibiretu
munthu woopa Mulungu. Ndiye ndimati mwina adzandipha chifukwa
cha mkazi wanga. 12 Komabe kunena zoona, iyeyu ndi mlongo wangadi,
mwana wamkazi wa abambo anga ngakhale kuti si ife a mayi mmodzi.
Tsono akhoza kukhala mkazi wanga. 13 Ndiye pamene Mulungu anati
ndichoke ku nyumba ya abambo anga, ndinawuza mkazi wangayu
kuti, ‘Kuti uwonetse kuti ndiwe mkazi wokoma mtima, uziwuza anthu
kulikonse kumene tingapite kuti ndine mlongo wako.’ ”
14 Tsono Abimeleki anapereka nkhosa, ng’ombe ndi antchito aamuna ndi
aakazi kwa Abrahamu. Ndipo anamubwezeranso Abrahamu Sara, mkazi
wake. 15 Tsono Abimeleki anati kwa Abrahamu, “Dziko langa ndi limene
ukulionali; ukhale paliponse pamene ufuna.”
16 Ndipo kwa Sara, iye anati, “Ndikumupatsa mlongo wakoyu makilo-
galamu khumi ndi awiri a siliva kutsimikiza kuti iwe ndi wosalakwa
pamaso pa onse amene ali ndi iwe; ulibedi mlandu.”
17 Tsono Abrahamu anapemphera kwa Mulungu ndipo Mulunguyo
anachiritsa Abimeleki, mkazi wake pamodzi ndi adzakazi ake kuti athenso
kubereka ana. 18 Paja Yehova n’kuti atatseka akazi onse a m’banja la
Abimeleki kuti asabereke ana chifukwa cha Sara, mkazi wa Abrahamu.

# 21

*Kubadwa kwa Isake*

1 Yehova anakomera mtima Sara monga ananenera, ndipo Yehovayo
anachita monga momwe analonjezera. 2 Sara anakhala ndi pathupi ndipo
anamuberekera Abrahamu mwana wamwamuna mu ukalamba wake, pa
nyengo imene Mulungu anamulonjeza. 3 Abrahamu anapereka dzina loti
Isake kwa mwana wamwamuna amene Sara anamuberekera. 4 Isake
atakwanitsa masiku asanu ndi atatu, Abrahamu anamuchita mdulidwe
monga Mulungu anamulamulira. 5 Abrahamu anali ndi 100 pamene
mwana wake Isake anabadwa.

[6] Sara anati, "Mulungu wandibweretsera mseko, ndipo aliyense amene
adzamva zimenezi adzaseka nane pamodzi." [7] Ndipo anawonjezera
kuti, "Ndani akanamuwuza Abrahamu kuti Sara n'kudzayamwitsako ana?
Chonsecho ndamubalira mwana wamwamuna kuwukalamba wake."

### *Kuchotsedwa kwa Hagara ndi Ismaeli*

[8] Mwana uja anakula mpaka kumuletsa kuyamwa. Tsiku lomuletsa Isake
kuyamwa, Abrahamu anakonza phwando lalikulu. [9] Koma Sara anaona
kuti mwana wamwamuna amene Hagara Mwigupto anamuberekera Abra-
hamu amamuseka, [10] ndipo anati kwa Abrahamu, "Muchotse mdzakazi
ndi mwana wake wamwamunayu, pakuti mwana wa kapolo sadzagawana
chuma ndi mwana wanga Isake."

[11] Nkhaniyi inamumvetsa chisoni kwambiri Abrahamu chifukwa
imakhudza mwana wake. [12] Koma Mulungu anamuwuza Abrahamu
kuti, "Usamve chisoni motero ndi mnyamatayu ndi mdzakazi wakoyu.
Mvetsera chilichonse chomwe Sara akukuwuza, chifukwa zidzukulu zako
zidzachokera mwa Isake. [13] Mwana wa mdzakazi wakoyu ndidzamusan-
dutsa mtundu wa anthu chifukwa ndi mwana wako."

[14] Mmamawa wake, Abrahamu anatenga chakudya ndi botolo la madzi
nazipereka kwa Hagara. Anasenzetsa Hagara nawaperekeza pang'ono
ndi mnyamatayo. Hagara ananyamuka nayendayenda m'chipululu cha
Beeriseba.

[15] Madzi atatha m'botolo muja, anamuyika mnyamatayo pansi pa
zitsamba. [16] Kenaka Hagara anachoka nakakhala pansi cha pakatalipo,
pafupifupi mamita makumi asanu ndi anayi, popeza m'maganizo mwake
amati, "Sindingaonerere mwanayu akufa." Ndipo anakhala pansi cha
poteropo n'kumalira.

[17] Mulungu anamva mnyamatayo akulira ndipo mngelo wa Mulungu
anayankhula kwa Hagara kuchokera kumwamba nati, "Chavuta n'chiyani
Hagara? Usachite mantha; Mulungu wamva kulira kwa mnyamatayo
pamene wagonapo. [18] Munyamule mnyamatayo ndipo umugwire dzanja
pakuti ndidzamupanga kukhala mtundu waukulu."

[19] Kenaka Mulungu anatsekula maso a Hagara ndipo anaona chitsime
cha madzi. Choncho anapita nadzaza botolo lija ndi madzi ndi kumupatsa
mnyamatayo kuti amwe.

[20] Mulungu anali ndi mnyamatayo pamene ankakula. Anakhala ku
chipululu nakhala katswiri wolasa uta. [21] Akukhala ku chipululu cha
Parani, mayi ake anamupezera mkazi wochokera ku Igupto.

### *Pangano la ku Beeriseba*

[22] Pa nthawiyo, Abimeleki ndi Fikolo wamkulu wankhondo wake anati
kwa Abrahamu, "Mulungu ali nawe pa chilichonse umachita. [23] Tsopano
undilumbirire ine pano pamaso pa Mulungu kuti sudzachita mwa
chinyengo ndi ine kapena ana anga kapena zidzukulu zanga. Undionetse
ine pamodzi ndi dziko limene ukukhalamo ngati mlendo, kukoma mtima
kokhala ngati kumene ndinakuonetsa ine."

[24] Abrahamu anati, "Ine ndikulumbira."

[25] Kenaka Abrahamu anadandaula kwa Abimeleki pa za chitsime
chimene antchito a Abimeleki analanda. [26] Koma Abimeleki anati,
"Ine sindikudziwa amene anachita zimenezi. Iwe sunandiwuze, ndipo
ndazimva lero zimenezi."

27 Choncho Abrahamu anabweretsa nkhosa ndi ng’ombe nazipereka
kwa Abimeleki, ndipo anthu awiriwo anachita pangano. 28 Abrahamu ana-
patulako ana ankhosa aakazi asanu ndi awiri kuchoka pagulu la nkhosa
zina, 29 ndipo Abimeleki anafunsa Abrahamu, “Kodi tanthauzo lake la
ana ankhosa aakazi asanu ndi awiri amene wawapatula pawokhawa
n’chiyani?”

30 Iye anayankha kuti, “Landirani ana ankhosa aakazi kuchokera
m’dzanja langa ngati umboni kuti ndinakumba chitsime ichi.”

31 Kotero malo amenewo anatchedwa Beeriseba, chifukwa anthu
awiriwo analumbirirapo malumbiro.

32 Atatha kuchita pangano pa Beeriseba, Abimeleki ndi Fikolo mkulu
wankhondo wake anabwerera ku dziko la Afilisti. 33 Abrahamu anadzala
mtengo wa bwemba ku Beeriseba, ndipo anapemphera pamenepo m’dzina
la Yehova, Mulungu Wamuyaya. 34 Ndipo Abrahamu anakhala m’dziko la
Afilisti kwa nthawi yayitali.

# 22

*Kuyesedwa kwa Abrahamu*

1 Nthawi ina zitatha izi, Mulungu anamuyesa Abrahamu. Iye anati,
“Abrahamu!”

Ndipo iye anayankha kuti, “Ee Ambuye.”

2 Ndipo Mulungu anati, “Tenga Isake, mwana wako yekhayo amene
umamukonda ndi kupita naye ku dziko la Moriya. Ukamupereke
iye ngati nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri a kumeneko limene
ndidzakuwuza.”

3 Abrahamu anadzuka mmamawa wake namangirira chokhalira pa
bulu. Atadula nkhuni zokwanira zowotchera nsembe yopsereza, Abra-
hamu, antchito ake awiri pamodzi ndi Isake ananyamuka kupita kumalo
kumene Mulungu anamuwuza Abrahamu. 4 Pa tsiku lachitatu, Abrahamu
anakweza maso ake ndipo anaona malowo chapatali. 5 Ndipo Abrahamu
anati kwa antchito ake aja, “Bakhalani pano ndi buluyu. Ine ndi
mnyamatayu tipita uko kukapemphera, koma tibweranso.”

6 Abrahamu anatenga nkhuni za nsembe yopsereza zija namusenzetsa
mwana wake Isake, ndipo iye mwini anatenga moto ndi mpeni. Pamene
awiriwo amayendera pamodzi, 7 Isake anati kwa abambo ake Abrahamu,
“Abambo?”

Abrahamu anayankha, “Ee mwana wanga.”

Isake anafunsa, “Moto ndi nkhuni zilipo, koma nanga mwana wankhosa
wa nsembe yopsereza ali kuti?”

8 Abrahamu anayankha, “Mwana wanga, Mulungu adzipezera yekha
mwana wankhosa wa nsembe yopsereza.” Ndipo awiriwo anapitiriza
ulendo.

9 Atafika pamalo pamene Mulungu anamuwuza paja, Abrahamu ana-
mangapo guwa lansembe nayika nkhuni pamwamba pa guwapo. Kenaka
anamumanga mwana wake Isake namugoneka paguwapo, pamwamba pa
nkhuni paja. 10 Kenaka Abrahamu anatambasula dzanja lake natenga
mpeni kuti aphe mwana wake. 11 Koma mngelo wa Yehova anayitana
Abrahamu kuchokera kumwamba nati, “Abrahamu! Abrahamu!”

Iye anayankha kuti, “Ee Ambuye.”

[12] Mngeloyo anati, “Usatambasulire mwanayo dzanja lako kuti umuphe,
pakuti tsopano ndadziwa kuti iwe umaopa Mulungu. Iwe sunandimane
mwana wako mmodzi yekhayo.”

[13] Abrahamu anatukula maso ake ndipo anaona nkhosa yamphongo
itakoledwa ndi nyanga zake mu ziyangoyango. Iye anapita nakatenga
nkhosa ija ndikuyipha ngati nsembe yopsereza m’malo mwa mwana
wake. [14] Choncho Abrahamu anatcha malo amenewa kuti Yehova-Yire
(Wopereka). Ndipo mpaka lero amatchula malowo kuti ndi “Pa phiri la
Yehova wopereka.”

[15] Mngelo wa Yehova anayitana Abrahamu kuchokera kumwamba
kachiwiri [16] ndipo anati, “Ndikulumbira mwa Ine ndekha kuti popeza
wachita zimenezi, wosandikaniza mwana wako mmodzi yekhayu,
[17] ndidzakudalitsa ndithu ndipo ndidzakupatsa zidzukulu zochuluka ngati
nyenyezi zamlengalenga komanso ngati mchenga wa m’mphepete mwa
nyanja. Zidzukulu zako zidzalanda mizinda ya adani awo, [18] ndipo
kudzera mwa chidzukulu chako, mitundu yonse ya anthu pa dziko lapansi
idzadalitsika, chifukwa iwe wandimvera.”

[19] Kenaka Abrahamu anabwerera kumene anasiya antchito ake kuja
nanyamukira nawo pamodzi kupita ku Beeriseba. Ndipo Abrahamu
anakhala ku Beeriseba.

### *Ana Aamuna a Nahori*

[20] Patapita nthawi, Abrahamu anamva kuti, “Milika nayenso anaberek-
era Nahori, m’bale wake ana. [21] Woyamba anali Huzi ndipo kenaka
m’bale wake Buzi. Anaberekanso Kemueli, amene anali abambo ake
a Aramu. [22] Ana ena ndi Kesede Hazo, Pilidasi, Yidilafi ndi Betueli.”
[23] Betueli anabereka Rebeka. Milika anaberekera Nahori, m’bale wake
wa Abrahamu, ana aamuna asanu ndi atatu amenewa. [24] Mkazi wake
wachiwiri, dzina lake Reuma, anamubaliranso Nahori ana awa: Teba,
Gahamu, Tahasi ndi Maaka.

## 23

### *Kumwalira kwa Sara*

[1] Sara anakhala ndi moyo zaka 127. [2] Anamwalirira ku Kiriyati-Araba,
kumeneku ndi ku Hebroni, m’dziko la Kanaani, ndipo Abrahamu anapita
kukakhuza maliro a Sara, namulirira.

[3] Kenaka Abrahamu ananyamuka pamene panali mtembo wa mkazi
wakepo kupita kukayankhula ndi anthu a ku Hiti. Ndipo anati, [4] “Ine
ndine mlendo wongoyendayenda kwanu kuno. Bwanji mundigulitse malo
woti akhale manda kuti ndiyikepo thupi la mkazi wanga.”

[5] Anthu a ku Hiti aja anamuyankha Abrahamu kuti, [6] “Tatimverani
mbuye wathu, inu ndinu mwana wa mfumu wamkulu pakati pathu.
Chonde ikani thupi la mkazi wanu m’manda aliwonse amene mungafune.
Palibe mmodzi wa ife amene adzakukanizani manda ake kuti musayike
mkazi wanu.”

[7] Tsono Abrahamu anayimirira naweramira anthu a dziko la Hiti
aja [8] nati, “Ngati mwaloladi kuti ndiyike mkazi wanga kuno, ndiye
ndimvereni. Mundipemphere kwa Efroni mwana wa Zohari [9] kuti
andigulitse phanga la Makipela, limene lili kumapeto kwa munda wake.
Mumupemphe kuti andigulitse pamtengo wake ndithu inu mukuona kuti
akhale manda.”

[10] Pamenepo n'kuti Efroni Mhiti ali pomwepo pakati pa anthuwo amene
anabwera ku chipata cha mzindawo. Ndipo onse akumva anamuyankha
Abrahamu [11] nati, "Ayi mbuye wanga tandimverani, ine ndikukupatsani
mundawo ndiponso phanga limene lili m'menemo. Ndikukupatsani
malowa pamaso pa anthu a mtundu wanga. Chonde ikani mtembo
wamkazi wanu."

[12] Apo Abrahamu anaweramanso mwaulemu pamaso pa anthu a
m'dzikolo [13] ndipo anthu onse akumva Abrahamu anati kwa Efroni, "Ngati
kungatheke, chonde ndimvereni. Ine ndichita kugula mundawu. Landi-
rani ndalama za mundawu kuti ine ndiyike mkazi wanga m'menemo."

[14] Koma Efroni anamuyankha Abrahamu nati, [15] "Mundimvere mbuye
wanga; mundawo mtengo wake ndi masekeli asiliva okwana 400. Koma
zimenezo n'chiyani pakati pa ine ndi inu? Ikani mtembo wa mkazi wanu."

[16] Abrahamu anavomera mtengo umene ananena Efroni Ahiti onse
akumva ndipo anamuwerengera masekeli asiliva okwana 400 monga mwa
mtengo wa ndalama umene amalonda a nthawi imeneyo ankagwiritsa
ntchito.

[17] Choncho munda wa Efroni wa ku Makipela umene unali kufupi
ndi Mamre, kuphatikiza munda, phanga linali m'menemo pamodzi ndi
mitengo yonse ya m'mundamo, zinaperekedwa [18] kwa Abrahamu ngati
chuma chake pamaso pa anthu onse a ku Hiti amene anabwera ku
chipata cha mzindawo. [19] Zitatha izi, Abrahamu anayika mkazi wake Sara
m'phanga la m'munda wa ku Makipela, kufupi ndi ku Mamre (kumene
ndi ku Hebroni) m'dziko la Kanaani. [20] Choncho Ahiti anapereka munda
pamodzi ndi phanga la m'menemo kwa Abrahamu kuti akhale manda.

# 24

*Isake ndi Rebeka*

[1] Tsopano Abrahamu anali atakalamba kwambiri, ndipo Yehova ana-
mudalitsa mu zonse anachita. [2] Tsiku lina Abrahamu anawuza wantchito
wake wamkulu amene ankayang'anira zonse anali nazo, kuti "Ika dzanja
lako pansi pa ntchafu yanga. [3] Ndikufuna kuti ulumbire pamaso pa
Yehova, Mulungu wakumwamba ndi dziko lapansi, kuti sudzamupezera
mwana wanga mkazi pakati pa atsikana Achikanaani a kuno kumene
ndikukhala, [4] koma kuti udzapita ku dziko la kwathu ndi kukamupezera
mkazi mwana wanga Isake pakati pa abale anga."

[5] Wantchito uja anafunsa kuti, "Nanga atakhala kuti mkaziyo sakufuna
kubwera nane kuno? Kodi ine ndingadzatenge mwana wanu ndi
kubwerera naye ku dziko kumene munachokera?"

[6] Abrahamu anati, "Uwonetsetse kuti usadzabwerere naye mwana
wanga kumeneko. [7] Yehova Mulungu wakumwamba amene ananditenga
kwa makolo anga nanditulutsa m'dziko lobadwira, ameneyo anayankhula
nane molumbira kuti, 'Kwa zidzukulu zako ndidzapereka dziko ili.' Iyeyu
adzatumiza mngelo wake kuti akutsogolere kumeneko kukapezera mwana
wanga mkazi. [8] Ngati mkaziyo adzakana kubwerera nawe ndiye kuti
udzakhala womasuka ku lumbiro langa. Koma usadzamutenge mwana
wanga ndi kubwerera naye kumeneko." [9] Choncho wantchitoyo anayika
dzanja lake pansi pa ntchafu ya mbuye wake Abrahamu nalumbira kwa
iye kuti adzachitadi monga mwa mawu a Abrahamu.

[10] Tsono wantchito uja anatengapo ngamira khumi mwa ngamira za
mbuye wake pamodzi ndi zinthu zabwino za mitundumitundu. Ndipo

ananyamuka kupita ku mzinda wa Nahori, m'dziko la Mesopotamiya.
11 Atafika, anagwaditsa pansi ngamira zija pafupi ndi chitsime chimene
chinali kunja kwa mzinda uja. Awa anali madzulo ndithu, nthawi imene
amayi amapita kukatunga madzi.

12 Ndipo wantchito uja anapemphera nati, "Haa, Yehova, Mulungu
wa mbuye wanga Abrahamu, mulole kuti zinthu zindiyendere ine lero,
ndipo muonetseni mbuye wanga Abrahamu kukoma mtima kwanu
kosasinthika. 13 Taonani ndayima pambali pa chitsimechi, ndipo atsikana
a mu mzindawu akubwera kudzatunga madzi. 14 Ine ndipempha
mtsikana wina kuti, 'Chonde tula mtsuko wako kuti ndimweko madzi.'
Tsono iye akayankha kuti 'Imwani,' ndipo ndidzapatsanso ngamira zanu
madziwo, ameneyo akhale mkazi amene mwasankhira mtumiki wanu
Isake." Zimenezi zikachitika, ndidzadziwa kuti mwaonetsadi kukoma
mtima kwanu kosasinthika kwa mbuye wanga.

15 Asanatsirize kupemphera, anangoona Rebeka watulukira atasenza
mtsuko wake pa phewa. Iyeyu anali mwana wa Betueli mwana wa
Milika, mkazi wa Nahori m'bale wake wa Abrahamu. 16 Mtsikanayo
anali wokongola kwambiri, namwali amene sanadziwe mwamuna. Iye
anatsikira ku chitsime nadzaza mtsuko nakweranso ku mtunda.

17 Wantchito uja anathamanga kukakumana naye nati, "Chonde patseko
madzi pang'ono a mu mtsuko wakowo kuti ndimwe."

18 Mtsikanayo anati, "Imwani mbuye wanga." Ndipo mofulumira
anatsitsa mtsuko uja nawuyika m'manja ndi kumupatsa kuti amwe.

19 Atatha kupereka madzi akumwa kwa mlendo uja, mtsikanayo
anati, "Ndikatungiranso ngamira madzi kuti zimwe mpaka zitakwana."
20 Choncho anafulumira kukhuthula madzi a mu mtsuko aja momwera
ziweto, nathamanga kubwerera ku chitsime kukatunga madzi ena, ndipo
anatunga okwanira ngamira zake zonse. 21 Modekha, munthu uja
anayang'anitsitsa kwambiri mtsikana uja kuti adziwedi ngati Yehova
anamutsogolera pa ulendo wake uja kapena ayi.

22 Ngamira zija zitatha kumwa, mlendo uja anatulutsa chipini chagolide
cholemera theka la sekeli ndi zibangiri zagolide ziwiri zolemera masekeli
100. 23 Kenaka anafunsa namwaliyo kuti, "Chonde tandiwuza, kodi ndiwe
mwana wa yani? Ndipo kodi malo alipo kwanu woti ife n'kugona?"

24 Anamuyankha kuti, "Ine ndine mwana wa Betueli, mwana amene
Milika anaberekera Nahori." 25 Ndipo anapitiriza kunena kuti, "Chakudya
chodyetsa nyamazi chilipo kwathu ndipo malo woti mugone aliponso."

26 Kenaka munthuyo anawerama pansi napembedza Yehova, 27 nati,
"Alemekezeke Yehova, Mulungu wa mbuye wanga Abrahamu, amene
waonetsa kukoma mtima kwake kosasintha ndi kukhulupirika kwake kwa
mbuye wanga. Yehova wanditsogolera pa ulendo wanga mpaka ndafika
ku nyumba kwa abale ake a mbuye wanga."

28 Mtsikana uja anathamanga nakafotokozera zimenezi anthu a kwa
amayi ake. 29 Tsono Rebeka anali ndi mlongo wake dzina lake Labani.
30 Iyeyu atangoona chipini pa mphuno ndi zibangiri pa mikono ya
mlongo wake komanso kumva zimene mlendo uja ananena kwa Rebekayo,
anathamangira kwa mlendo uja, ndipo anamupeza atangoyima ndi
ngamira zake pafupi ndi chitsime. 31 Iye anati, "Tiyeni kwathu, ndinu
munthu amene Yehova wamudalitsa. Bwanji mwangoyimirira panja
pano? Ine ndakukonzerani malo ogona inu ndi ngamira zanu."

32 Choncho munthu uja analowa m'nyumba. Labani anatsitsa katundu
anali pa ngamira uja. Kenaka anazipatsa ngamira zija chakudya, ndiponso

anapereka madzi wosamba mapazi kwa mlendo uja ndi anthu ena
onse. 33 Chakudya chitabwera mlendo uja anati, “Sindidya mpaka
nditakuwuzani zimene ndadzera kuno.”

Labani anati, “Yankhulani.”

34 Motero iye anati, “Ine ndine wantchito wa Abrahamu. 35 Yehova
wadalitsa mbuye wanga kwambiri, ndiponso walemera. Wamupatsa
nkhosa ndi ng’ombe, siliva ndi golide, antchito aamuna ndi antchito
aakazi, komanso ngamira ndi abulu. 36 Sara, mkazi wa mbuye
wanga anamubalira iye mwana wamwamuna ngakhale kuti Sarayo anali
wokalamba. Tsono mbuye wanga wamupatsa mwanayo chuma chonse.
37 Tsono mbuye wanga anandilumbiritsa kuti ndisunge mawu ake akuti,
‘Usadzamupezere mwana wanga mkazi kuchokera mwa atsikana a dziko
lino la Kanaani, 38 koma upite ku banja la abambo anga ndi kwa abale
anga kuti ukamupezere mkazi mwana wanga.’ ”

39 “Ndipo ine ndinati kwa mbuye wanga, ‘Nanga mkaziyo akakapanda
kubwera nane pamodzi?’

40 “Iye anayankha, ‘Yehova amene ndakhala ndikumumvera nthawi
zonse, adzatumiza mngelo wake kuti akuperekeze ndipo adzakuthandiza
mpaka ukamupezere mwana wanga mkazi kuchokera ku mtundu wanga,
wa fuko langa. 41 Ukadzachita zimenezi udzakhala mfulu wosamangidwa
ndi lumbiro langali. Koma tsono ukadzafika kwa fuko langa, ndipo ngati
sadzalola kukupatsa mbeta ya mwana wanga, aponso udzamasuka ku
lumbiro langali.’ ”

42 “Tsono lero lino pamene ndafika pa chitsime, ndinapempha kuti,
‘Yehova, Mulungu wa mbuye wanga, Abrahamu, ngati Inu mwandi-
dalitsadi pa ulendowu, 43 taonani ndayima pambali pa chitsime ichi;
ndipo ndidzati kwa namwali amene atabwere kudzatunga kuti, chonde
nditamwako madzi a mu mtsuko wakowu,’ 44 ndipo ngati adzandiyankha
kuti, ‘Imwani ndipo ndizimwetsanso madzi ngamira zanuzi,’ ameneyo
akhale yemwe Yehova wamusankhira mwana wa mbuye wanga.”

45 “Ndisanatsirize kupemphera, ndinangoona Rebeka akutulukira mt-
suko wake uli pa phewa. Anatsetserekera ku chitsime kukatunga madzi
ndipo ndinati kwa iye, ‘Chonde patseko madzi akumwa.’

46 “Mofulumira, anatsitsa mtsuko wake pa phewa pake nati, ‘Imwani
ndiponso ndizimwetsa madzi ngamira zanuzi.’ Kotero ine ndinamwa
ndipo anamwetsanso ngamirazo.

47 “Ndinamufunsa kuti, ‘Ndiwe mwana wa yani?’

“Iye anati, ‘Ndine mwana wa Betueli mwana wa Nahori, amene Milika
anamuberekera.’

“Tsono ndinayika chipini pa mphuno yake ndi kumveka zibangiri
m’mikono yake, 48 kenaka ndinawerama pansi ndi kupembedza Yehova.
Ndipo ndinatamanda Yehova, Mulungu wa mbuye wanga Abrahamu,
amene anandilondolera mokhulupirika njira yanga. Iye wandifikitsa kwa
m’bale wake kumene ndapezera mbeta mwana wa mbuye wanga. 49 Tsono
ngati mukufuna kuonetsa kukoma mtima kwanu kwa mbuye wanga,
ndikuonetsa kukhulupirika kwanu, ndiwuzeni; ndipo ngati si choncho
ndiwuzeninso kuti ndidziwe chochita.”

50 Labani ndi Betueli anayankha nati, “Izi ndi zochokera kwa Yehova,
ndipo ife sitinganenepo kanthu. 51 Nayu Rebeka, mutengeni muzipita
naye kuti akakhale mkazi wa mwana wa mbuye wanu, monga Yehova
wanenera.”

52 Wantchito wa Abrahamu uja atamva zimene anawerama pansi
pamaso pa Yehova. 53 Kenaka wantchitoyo anatulutsa ziwiya zagolide
ndi zasiliva ndi zovala nazipereka kwa Rebeka. Anaperekanso mphatso
zina za mtengowapatali kwa mlongo wake ndi amayi ake a Rebeka.
54 Tsono wantchito uja ndi anthu amene anali naye anadya, kumwa
nagona komweko.

Kutacha mmawa wake, wantchito uja anati, "Mundilole ndibwerere kwa mbuye wanga."

55 Koma mlongo wake ndi amayi ake a Rebeka anayankha kuti, "Muloleni mtsikanayu abakhala nafe masiku khumi kapena kupyolerapo, kenaka mukhoza kupita."

56 Koma iye anawawuza kuti, "Chonde musandichedwetse. Yehova wandithandiza kale pa ulendo wanga. Mundilole ndibwerere kwa mbuye wanga."

57 Koma iwo anati, "Bwanji timuyitane mtsikanayo ndipo timufunse
ngati afuna kupita nanu panopa." 58 Choncho iwo anamuyitana Rebeka
uja namufunsa kuti, "Kodi ukufuna kupita ndi munthuyu panopa?"

Iye anayankha kuti, "Ndipita."

59 Kotero anamulola Rebeka pamodzi ndi mlezi wake kuti apite ndi
wantchito wa Abrahamu pamodzi ndi anthu amene anali naye. 60 Ndipo
iwo anadalitsa Rebeka ndi kumuwuza kuti,

"Iwe ndiwe mlongo wathu, Mulungu akudalitse iwe, ukhale
    mayi wa anthu miyandamiyanda;
ndi kuti zidzukulu zako zidzalanda
    mizinda ya adani awo."

61 Kenaka Rebeka ndi antchito ake ananyamuka kukakwera ngamira zawo ndipo anapita naye pamodzi munthu uja. Choncho wantchito uja anatenga Rebeka n'kumapita.

62 Pa nthawiyi n'kuti Isake atafika kuchokera ku chitsime cha Wamoyo
Wondipenya (Beeri-lahai-roi), popeza tsopano ankakhala ku Negevi.
63 Tsiku lina chakumadzulo, Isake anatuluka kukayendayenda ku munda,
ndipo atakweza maso anaona ngamira zikubwera. 64 Rebeka nayenso
anatukula maso naona Isake. Ndipo anatsika pa ngamira yake 65 nafunsa
wantchito uja kuti, "Kodi munthu uyo ndi ndani akuyenda m'mundamo kubwera kudzakumana nafe?"

Wantchitoyo anayankha, "Ndiye mbuye wanga." Choncho Rebeka anatenga nsalu ndi kufunda kumaso.

66 Tsono wantchito uja anawuza Isake zonse zimene anazichita. 67 Isake
analowa naye Rebeka mu tenti ya amayi ake Sara, ndipo anakhala mkazi wake. Isake anamukonda kwambiri Rebeka mkazi wake motero kuti zimenezi zinamutonthoza imfa ya amayi ake.

# 25

*Abrahamu Amwalira*

1 Abrahamu anakwatira mkazi wina dzina lake Ketura. 2 Iyeyu
anamubalira Zimurani, Yokisani, Medani, Midiyani, Isibaki ndi Suwa.
3 Yokisani anabereka Seba ndi Dedani ndipo zidzukulu za Dedani ndiwo
Aasuri, Aletusi, ndi Aleumi. 4 Ana aamuna a Midiyani anali, Efai, Eferi,
Hanoki, Abida ndi Elida. Onsewa anali zidzukulu za Ketura.

5 Abrahamu anasiyira Isake chilichonse anali nacho. 6 Koma pamene
anali ndi moyo, Abrahamu anapereka mphatso kwa ana aakazi ake ena

onse. Kenaka anawatumiza ku dziko la kummawa kuti akhale kutali ndi
mwana wake Isake.
7 Abrahamu anakhala ndi moyo zaka 175. 8 Abrahamu anamwalira
atakalamba kwambiri ndipo anakakhala ndi anthu a mtundu wake. 9 Ana
ake, Isake ndi Ismaeli anamuyika m'phanga la Makipela pafupi ndi
Mamre, m'munda umene kale unali wa Efroni mwana wa Zohari Mhiti,
10 uwu ndi munda umene Abrahamu anagula kwa Ahiti. Kumeneko
Abrahamu anakayikidwa pamodzi ndi mkazi wake Sara. 11 Atamwalira
Abrahamu, Mulungu anadalitsa mwana wake Isake, amene ankakhala
pafupi ndi Beeri-lahai-roi (chitsime cha Wamoyo Wondipenya).

### *Ana Aamuna a Ismaeli*

12 Nazi zidzukulu za Ismaeli, mwana wa Abrahamu amene wantchito
wa Sara, Hagara Mwigupto uja, anaberekera Abrahamu.

13 Awa ndi mayina a ana a Ismaeli monga mwa mndandanda wa
mabadwidwe awo: Nebayoti ndiye anali mwana woyamba wa Ismaeli;
kenaka Kedara, Adibeeli, Mibisamu, 14 Misima, Duma, Masa, 15 Hadadi,
Tema, Yeturi, Nafisi ndi Kedema; 16 Amenewa ndi ana a Ismaeli ndi mayina
awo monga mwa midzi ndi misasa yawo. Anali olamulira mafuko khumi
ndi awiri. 17 Ismaeli anakhala ndi moyo zaka 137. Iye anamwalira ndipo
anakakhala ndi anthu a mtundu wake. 18 Zidzukulu za Ismaeli zinkakhala
m'dera la pakati pa Havila ndi Suri, kummwera kwa Igupto, mukamapita
cha ku Asuri. Choncho anakhala kummawa kwa abale awo.

### *Yakobo ndi Esau*

19 Iyi ndi mbiri ya Isake mwana wa Abrahamu.

Abrahamu anabereka Isake 20 ndipo Isake anali ndi zaka makumi
anayi pamene anakwatira Rebeka mwana wa Betueli Mwaramu wa ku
Padanaramu mlongo wa Labani Mwaramu.
21 Isake anapempherera mkazi wake kwa Yehova popeza iye anali
wosabereka. Yehova anayankha pemphero lake ndipo mkazi wake Rebeka
anatenga pathupi. 22 Koma pamene anawo amalimbana m'mimba mwake,
iye anati, “Bwanji zikundichitikira zoterezi?” Choncho anapita kukafunsa
kwa Yehova.
23 Yehova anati kwa iye,

“Udzabala mafuko awiri a anthu olimbana,
    ndipo magulu awiri a anthu ochokera mwa iwe adzasiyana;
fuko limodzi lidzakhala la mphamvu kuposa linzake,
    ndipo wamkulu adzatumikira wamng'ono.”

24 Pamene nthawi inakwana yakuti abeleke, Rebeka anaberekadi ma-
pasa. 25 Woyamba kubadwa anali wofiira, ndipo thupi lake lonse linali
ngati chovala cha ubweya; choncho anamutcha Esau. 26 Kenaka m'bale
wake anabadwa atagwira chidendene cha Esau; choncho anamutcha
Yakobo. Isake anali ndi zaka 60 pamene Rebeka anabereka mapasawa.
27 Anyamatawo anakula ndipo Esau anakhala katswiri wosaka, munthu
wam'thengo, pamene Yakobo anali munthu wofatsa, wokonda kukhala pa
nyumba. 28 Isake ankakonda Esau chifukwa cha nyama za kutchire zomwe
ankakonda kudya, koma Rebeka ankakonda Yakobo.
29 Tsiku lina pamene Yakobo ankaphika chakudya, Esau anabwera
kuchokera kuthengo ali wolefuka ndi njala. 30 Iye anati kwa Yakobo,

"Tandipatsako phala lofiiralo, ndimwe! Ndalefuka ndi njala." (N'chifukwa
chake amatchedwanso Edomu).
31 Yakobo anayankha, "Choyamba undigulitse ukulu wako."
32 Esau anati, "Chabwino, ine ndatsala pang'ono kufa, ukulu un-
dithandiza chiyani?"
33 Koma Yakobo anati, "Lumbira kwa ine choyamba." Kotero Esau
analumbiradi, ndipo anagulitsa ukulu wake kwa Yakobo.
34 Choncho Yakobo anamupatsa Esau buledi ndi phala lofiira lija. Iye
anadya ndi kumwa, nanyamuka kumapita.
Motero Esau anapeputsa ukulu wake wachisamba uja.

# 26

*Isake ndi Abimeleki*
1 Tsono kunagwa njala ina m'dzikomo kuwonjezera pa ija ya poyamba
ya nthawi ya Abrahamu ndipo Isake anapita kwa Abimeleki mfumu ya
Afilisti ku Gerari. 2 Yehova anadza kwa Isake nati, "Usapite ku Igupto;
koma ukhale m'dziko limene ndidzakuwuza kuti ukakhalemo. 3 Khala
m'dziko lino ndipo ndidzakhala nawe ndi kukudalitsa. Pakuti kwa iwe ndi
zidzukulu zako ndidzapereka mayiko onsewa. Choncho ndidzakwaniritsa
pangano limene ndinalumbira kwa Abrahamu, abambo ako. 4 Zidzukulu
zako ndidzazichulukitsa ngati nyenyezi za mu mlengalenga ndi kuzipatsa
mayiko onsewa. Ndiponso anthu onse a pa dziko lapansi adzadalitsika
kudzera mwa zidzukulu zako, 5 chifukwa Abrahamu anandimvera, na-
sunga malamulo anga onse." 6 Choncho Isake anakhala ku Gerari.
7 Anthu akumaloko atafunsa Isake za mkazi wake, iye anati, "Ndi
mlongo wanga ameneyu." Iye anaopa kunena kuti, "Ndi mkazi wanga
ameneyu," popeza ankaganiza kuti anthu akumeneku akhoza kumupha
ndi kukwatira mkazi wake popeza Rebeka anali wokongola.
8 Isake atakhalako kumeneko nthawi yayitali, Abimeleki mfumu ya
Afilisti, anasuzumira pa zenera kuyang'ana kunja, ndipo anaona Isake
akugwiragwira Rebeka, mkazi wake. 9 Choncho Abimeleki anamuyitanitsa
Isake nati, "Uyu ndi mkazi wako ndithu! Nanga bwanji umati, 'Ndi mlongo
wanga'?"
Ndipo Isake anamuyankha kuti, "Ine ndimaganiza kuti ndingataye moyo
wanga chifukwa cha iyeyu."
10 Tsono Abimeleki anati, "N'chiyani chimene watichitira? Mmodzi mwa
anthuwa anatsala pang'ono kugona ndi mkazi wako ndipo ukanatisan-
dutsa ife kukhala olakwa."
11 Choncho Abimeleki analamula anthu ake onse nati, "Aliyense amene
avutitse munthu uyu pamodzi ndi mkazi wake adzaphedwa ndithu."
12 Isake anadzala mbewu m'munda, ndipo chaka chomwecho anakolola
zinthu zambiri chifukwa Yehova anamudalitsa. 13 Isake analemera.
Chuma chake chinkachulukirachulukira mpaka anasanduka munthu
wolemera kwambiri. 14 Anali ndi nkhosa, ng'ombe ndi antchito ambiri
mwakuti Afilisti anamuchitira nsanje. 15 Nthawi iyi n'kuti Afilisti
atakwirira ndi dothi zitsime zonse zimene antchito abambo ake Abrahamu
anakumba mu nthawi ya abambo akewo.
16 Ndipo Abimeleki anati kwa Isake, "Muchoke pakati pathu chifukwa
mwasanduka wamphamvu kuposa ife."
17 Choncho Isake anachokako kumeneko nakakhala ku chigwa cha
Gerari kumene anakhazikikako. 18 Isake anafukulanso zitsime zija zimene

zinakumbidwa mu nthawi ya abambo ake Abrahamu. Atamwalira Abra-
hamu, Afilisti anakwirira zitsimezi. Tsono anazitcha mayina omwewo
amene abambo ake anazitcha.
19 Antchito a Isake anakumba m'chigwamo ndipo anapezamo kasupe
wa madzi. 20 Koma abusa a ku Gerari anakangana ndi abusa a Isake
nati, "Madziwa ndi athu." Motero iye anachitcha chitsimecho Mkangano
chifukwa anakangana naye. 21 Kenaka iwo anakumba chitsime china,
koma anakangananso chifukwa cha chitsimecho. Choncho anachitcha
dzina lakuti Chidani. 22 Anachokapo pamenepo nakakumba china. Koma
apa sanakanganiranenso ndi munthu. Iye anachitcha Kutakasuka, nati,
"Tsopano Yehova watipatsa ife malo otakasukirako ndipo tilemera muno."
23 Kenaka Isake anachoka ku malo kuja kupita ku Beeriseba. 24 Usiku
umenewo Yehova anadza kwa Isake nati, "Ine ndine Mulungu wa
abambo ako Abrahamu. Usachite mantha popeza Ine ndili ndi iwe.
Ndidzakudalitsa ndipo ndidzakupatsa zidzukulu zambiri chifukwa cha
mtumiki wanga Abrahamu."
25 Isake anamanga guwa lansembe pamenepo ndipo anapembedza
Yehova. Pomwepo anamanga tenti yake, ndipo antchito ake anakumba
chitsime.
26 Abimeleki pamodzi ndi Ahuzati mlangizi wake ndi Fikolo mkulu wa
ankhondo ake anabwera kwa Isake kuchokera ku Gerari. 27 Tsopano Isake
anawafunsa kuti, "Bwanji mwabwera kwa ine, popeza munandichitira
nkhanza ndi kundithamangitsa?"
28 Iwo anayankha, "Tsopano tadziwa kuti Yehova anali ndi iwe; ndiye
taganiza kuti inu ndi ife tichite lumbiro. Ife tichite pangano ndi inu 29 kuti
inu simudzatichitira zoyipa monga ifenso sitinakuchitireni nkhondo. Ife
tinakuchitirani zabwino zokhazokha, ndipo tinakulolani kuti musamuke
kuchoka kwathu mu mtendere. Tsopano Yehova wakudalitsani."
30 Tsono Isake anawakonzera phwando, ndipo anadya ndi kumwa.
31 Mmawa wake aliyense analumbira pangano kwa mnzake. Tsono Isake
anawalola kuti anyamuke ndipo anamusiya mu mtendere.
32 Tsiku limenelo, antchito a Isake anabwera namuwuza za chitsime
chimene anakumba. Iwo anati, "Tawapeza madzi!" 33 Iye chitsimecho
anachitcha Pangano. N'chifukwa chake mzindawu umatchedwa Beeriseba
mpaka lero.
34 Pamene Esau anali ndi zaka 40, anakwatira Yuditi mwana wamkazi
wa Beeri Mhiti. Anakwatiranso Basemati mwana wa mkazi wa Eloni Mhiti.
35 Akazi awiriwa anasandutsa Isake ndi Rebeka kukhala ndi moyo wa
madandawulo nthawi zonse.

# 27

### *Yakobo Alandira Madalitso kwa Isake*

1 Isake atakalamba maso ake anachita khungu mwakuti sankatha kuona.
Iye anayitana mwana wake wamkulu Esau nati kwa iye, "Mwana wanga."
Iye anayankha, "Ine abambo."
2 Isake anati, "Tsopano ine ndakalamba, ndipo sindidziwa tsiku langa
lakufa. 3 Tsono tenga zida zako, muvi wako ndi uta, pita kuthengo
ukandiphere nyama. 4 Undikonzere chakudya chabwino monga muja
ndimakonderamu ndipo ubwere nacho kwa ine kuti ndidye ndi kuti
ndikudalitse ndisanamwalire."

5 Koma Rebeka amamvetsera pamene Isake amayankhula ndi mwana
wake Esau. Esau atanyamuka kupita kuthengo kukaphera abambo ake
nyama, 6 Rebeka anati kwa mwana wake Yakobo, “Taona ndamva abambo
ako akuwuza m’bale wako Esau kuti, 7 ‘Bweretsere nyama yakutchire
ndipo undikonzere chakudya chokoma kuti ndidye; kuti ndikudalitse
pamaso pa Yehova ndisanamwalire.’ 8 Tsopano mwana wanga, mvetsetsa
ndipo uchite zimene ndikuwuze: 9 Pita ku khola, ukatenge ana ambuzi
abwino awiri, kuti ndikonzere abambo ako chakudya chokoma monga
amakondera. 10 Kenaka upite nacho chakudyacho kwa abambo ako kuti
adye ndi kukudalitsa asanafe.”

11 Koma Yakobo anati kwa Rebeka amayi ake, “Komatu m’bale wanga
Esau ndi munthu wa khungu la ubweya zedi, ndipo ine ndine munthu wa
khungu losalala. 12 Mwina abambo anga adzandikhudza, ndipo ndidza-
oneka kuti ndawapusitsa. Tsono ndizadzitengera temberero m’malo mwa
madalitso.”

13 Amayi ake anati kwa iye, “Mwana wanga, temberero limenelo
ligwere ine. Iwe ungochita zimene ine ndikukuwuza; pita kanditengere
timbuzito.”

14 Choncho anapita nakatenga timbuzito ndi kubwera nato kwa amayi
ake. Choncho Rebeka anaphika chakudya chokoma monga momwe
Isake amakondera. 15 Tsono Rebeka anatenga zovala zabwino kwambiri
za Esau mwana wake wamkulu zimene zinali m’nyumba namuveka
Yakobo. 16 Anamuvekanso manja ake ndi khosi lake ndi zikopa za
mwana wambuzi. 17 Kenaka, anamupatsa Yakobo chakudya chokoma
chija chimene anaphika pamodzi ndi buledi.

18 Yakobo anapita kwa abambo ake ndipo anati, “Abambo anga.”

Ndipo anayankha, “Eya, kodi ndiwe mwana wanga uti?”

19 Yakobo anati kwa abambo ake, “Ndine Esau mwana wanu woyamba.
Ndachita monga munandiwuzira. Chonde dzukani ndi kukhala tsonga kuti
mudyeko nyama ndakukonzeraniyi kuti tsono mundidalitse.”

20 Isake anafunsa mwana wake, “Wayipeza msanga chotere bwanji
mwana wanga?”

Iye anayankha, “Yehova Mulungu wanu ananandithandiza kuti ndiyipeze.”

21 Pamenepo Isake anati kwa Yakobo, “Tabwera pafupi ndikukhudze
mwana wanga, kuti ndidziwedi ngati uli mwana wanga Esau kapena ayi.”

22 Yakobo anasendera kufupi ndi abambo ake Isake ndipo anamukhudza
nati, “Mawuwa ndi mawu a Yakobo koma mikonoyi ndi mikono ya Esau.”
23 Sanamuzindikire, popeza mikono yake inali ndi ubweya ngati ya m’bale
wake Esau; choncho anamudalitsa. 24 Isake anafunsa, “Kodi ndiwedi
mwana wanga Esau?”

Yakobo anayankha, “Inde ndine.”

25 Ndipo iye anati, “Mwana wanga, patseko nyama yakoyo ndidye kuti
ndikudalitse.”

Yakobo anabwera ndi nyama ija kwa Isake ndipo anadya. Kenaka
anamupatsanso vinyo ndipo anamwa. 26 Tsono Isake anati kwa Yakobo,
“Bwera kuno mwana wanga undipsompsone.”

27 Choncho anapita namupsompsona. Apa Isake anamva fungo la zovala
zake, ndipo anamudalitsa nati,

“Haa, fungo la mwana wanga
lili ngati fungo la munda
umene Yehova waudalitsa.

28 Mulungu akugwetsere mame akumwamba
ndipo minda yako ibale tirigu wambiri
ndi vinyo watsopano.
29 Mitundu ya anthu ikutumikire iwe
ndipo anthu akugwadire iwe.
Ukhale wolamula abale ako,
ndipo ana aamuna a amayi ako akugwadire.
Amene akutemberera iwe atembereredwe
ndipo amene adalitsa iwe adalitsike."

30 Isake atatsiriza kudalitsa Yakobo, atangochoka pamaso pa abambo
akewo, Esau anabwera kuchokera kosaka kuja. 31 Nayenso anakonza
chakudya chokoma nabwera nacho kwa abambo ake. Ndipo anati kwa
iye, "Chonde abambo, dzukani mukhale tsonga kuti mudye nyamayi ndi
kuti mundidalitse."

32 Abambo ake, Isake, anamufunsa kuti, "Ndiwe yani?"

Iye anayankha, "Ndine mwana wanu woyamba Esau."

33 Isake ananjenjemera kwambiri nati, "Nanga ndani uja anakapha
nyama kutchire n'kudzandipatsa? Ine ndadya kale, ndadya nyamayo iwe
utangotsala pang'ono kubwera ndipo ndamudalitsa ndipo adzakhaladi
wodalitsika."

34 Esau atamva mawu a abambo ake, analira mokweza ndi mowawidwa
mtima nati kwa abambo ake, "Inenso dalitseni abambo anga!"

35 Koma iye anati, "M'bale wako anabwera mwachinyengo ndipo
watenga madalitso ako."

36 Esau anati, "Kodi n'chifukwa chake iyeyu dzina lake lili Yakobo eti?
Aka n'kachiwiri kundinyenga: Anatenga ukulu wanga, pano watenga
madalitso anga!" Kenaka anafunsa, "Kodi simunandisungireko ena
madalitsowo?"

37 Koma Isake anamuyankha nati, "Ndamudalitsa iye kuti akhale
wokulamulira iwe. Ndaperekanso abale ake onse kuti akhale omutumikira
iye, ndipo ndamudalitsa ndi tirigu wambiri, ndi vinyo watsopano. Ndiye
ndingakuchitirenso chiyani mwana wanga?"

38 Esau anati kwa abambo ake, "Kodi muli ndi dalitso limodzi lokhali,
abambo anga? Inenso mundidalitse chonde abambo anga!" Pomwepo
Esau analira mokuwa.

39 Tsono Isake abambo ake anamuyankha kuti,
"Malo ako okhalapo
sadzabala dzinthu,
ndipo mvula sidzagwa pa minda yako.
40 Udzakhala ndi moyo podalira lupanga
ndipo udzatumikira m'bale wako.
Koma idzafika nthawi
pamene udzakhala mfulu
udzachotsa goli lake m'khosi mwako."

### *Yakobo Athawira kwa Labani*

41 Ndipo Esau anamusungira chiwembu Yakobo chifukwa cha madalitso
amene abambo ake anamupatsa. Esau anati kwa iye yekha, "Masiku olira
abambo anga ayandikira; pambuyo pake ndidzamupha m'bale wangayu
Yakobo."

42 Pamene Rebeka anamva zimene mwana wake wamkulu Esau anka-
ganiza, anayitanitsa Yakobo nati kwa iye, "M'bale wako Esau akulingalira
zakuti akuphe kuti akulipsire. 43 Tsopano mwana wanga, chita zimene
ndinene: Nyamuka tsopano, uthawire kwa mlongo wanga Labani ku

Harani. 44 Ukakhale naye kwa kanthawi mpaka mkwiyo wa m'bale
wako utatsika. 45 Tsono mkwiyo wa m'bale wakoyo ukadzatsika ndi
kuyiwala zonse wamuchitirazi, ndidzatuma munthu kuti adzakutenge.
Nanga nditayirenji nonse awiri nthawi imodzi?"

46 Tsono Rebeka anati kwa Isake, "Ine sindikukondwera nawo anamwali
a Chihiti. Ndipo ngati Yakobo angapeze mbeta kuno mwa anamwali a
Chihitiwa, ndiye kuli bwino kungofa."

# 28

1 Choncho Isake anayitanitsa Yakobo namudalitsa n'kumuwuzitsa kuti,
"Usakwatire mkazi wa kuno ku Kanaani. 2 Panopo upite ku Pada-
naramu, ku nyumba kwa Betueli abambo a amayi akowa, kumeneko
ukakwatire mmodzi mwa ana aakazi a Labani, mlongo wa amayi akowa.
3 Mulungu Wamphamvuzonse akudalitse iwe nakupatse ana ambiri
mpaka udzasanduke gulu lalikulu la mitundu ya anthu. 4 Mulunguyo
akudalitse iwe monga mmene anamudalitsira Abrahamu kuti zidzukulu
zako zidzalandira dziko limene ukukhalamo ngati mlendo kuti lidzakhale
lawo. Ili ndi dziko limene Mulungu anapereka kwa Abrahamu." 5 Ndipo
Isake anamulola Yakobo kuti anyamuke kupita ku Padanaramu kwa
Labani mwana wa Betueli Mwaramu. Labani anali mlongo wa Rebeka,
mayi wa Yakobo ndi Esau.

6 Tsopano Esau anadziwa kuti Isake anadalitsa Yakobo ndi kumutumiza
ku Padanaramu kuti akakwatire kumeneko. Anawuzidwanso kuti, "Usak-
watire mkazi wa ku Kanaani." 7 Yakobo anamvera abambo ake ndi amayi
ake ndi kupita ku Padanaramu. 8 Ndiye pamenepo Esau anazindikira kuti
abambo ake Isake sankakondwera ndi akazi a ku Kanaani; 9 anapita kwa
Ismaeli mwana wa Abrahamu nakwatira Mahalati mwana wa Ismaeli,
mlongo wake wa Nebayoti. Anatero kuwonjezera akazi amene anali nawo
kale.

### *Maloto a Yakobo pa Beteli*

10 Yakobo ananyamuka pa ulendo kuchoka ku Beeriseba kupita ku
Harani. 11 Atafika pa malo pena, anayima kuti agonepo chifukwa dzuwa
linali litalowa. Anatenga mwala wina pomwepo natsamiritsapo mutu
wake, ndipo anagona. 12 M'maloto, anaona makwerero oyimikidwa
pansi ndipo anakafika kumwamba. Angelo a Mulungu amakwera ndi
kutsika pa makwereropo. 13 Tsono Yehova anayimirira pambali pake,
nati, "Ine ndine Yehova, Mulungu wa Abrahamu kholo lake la Isake
abambo ako. Ndidzakupatsa iwe ndi zidzukulu zako dziko limene
ukugonamolo. 14 Zidzukulu zako zidzachuluka ngati fumbi la pa dziko
lapansi ndipo zidzabalalikira kumadzulo ndi kummawa, kumpoto ndi
kummwera. Anthu onse adzalandira madalitso kudzera mwa iwe ndi
zidzukulu zako. 15 Ine ndili nawe pamodzi ndipo ndidzakuyang'anira
kulikonse upiteko, ndipo ndidzakubwezera ku dziko lino. Sindidzakusiya
mpaka nditachita zimene ndakulonjezazi."

16 Yakobo atadzidzimuka, anati, "Zoonadi Yehova ali pa malo ano, ndipo
ine sindinadziwe." 17 Tsono anachita mantha ndipo anati, "Malo ano ndi
woopsa ndithu. Zoonadi pano ndi pa nyumba ya Mulungu ndi khomo la
kumwamba."

18 Mmamawa mwake Yakobo anatenga mwala umene anatsamira mutu
wake uja nawuyimika ngati chipilala ndi kuthira mafuta pamwamba

pake 19 Iye anawatcha malowo Beteli, ngakhale kuti poyamba mzindawo
ankawutcha Luzi.
20 Pamenepo Yakobo analumbira kwa Yehova nati, “Ngati inu Mulungu
mukhala ndi ine, kundiyang’anira pa ulendo wangawu ndi kundipatsa
chakudya ndi chovala; 21 ngati inu mudzandibweretsa kwathu mu
mtendere, ndiye kuti mudzakhala Mulungu wanga, 22 ndipo mwala uwu
ndawuyimikawu udzakhala Nyumba ya Mulungu. Ine ndidzakupatsani
chakhumi cha zinthu zonse zimene mudzandipatse.”

# 29

*Yakobo Afika ku Padanaramu*

1 Yakobo anapitiriza ulendo wake kupita ku dziko la anthu a kummawa.
2 Atafika kumeneko anaona chitsime ku busa ndipo panali magulu
atatu a nkhosa zitagona pafupi ndi chitsimecho chifukwa nkhosazo
zimamwetsedwa madzi ochokera m’chitsimecho. Pamwamba pa chitsime-
cho panali mwala waukulu. 3 Amati nkhosa zonse zikasonkhana, abusawo
ankagudubuza mwalawo, kuwuchotsa ndi kumwetsa madzi nkhosazo.
Kenaka ankawubwezera mwalawo pamalo pake, pakamwa pa chitsimepo.
4 Yakobo anafunsa abusawo kuti, “Abale anga, mwachokera kuti?”
Iwo anayankha, “Tachokera ku Harani.”
5 Iye anawafunsanso kuti, “Kodi Labani, mdzukulu wa Nahori muku-
mudziwa?”
Iwo anayankha, “Inde tikumudziwa?”
6 Ndipo Yakobo anawafunsanso, “Kodi ali bwino?”
Iwo anati, “Inde ali bwino. Nayu Rakele mwana wake akubwera apoyu
ndi nkhosa.”
7 Iye anati, “Taonani, dzuwa likanalipo ndipo nthawi yosonkhanitsa
nkhosa sinakwane. Bwanji osazimwetsa madzi nkhosazi.”
8 Iwo anayankha, “Ayi sitingatero. Tidikira mpaka nkhosa zonse
zisonkhane. Zikatero, tigubuduza mwalawu kuwuchotsa pamwamba pa
chitsimepo, kenaka n’kuzimwetsa madzi nkhosazo.”
9 Ali chiyankhulire nawo, Rakele anafika ndi nkhosa za abambo ake
popeza ndiye amene ankaweta nkhosazo. 10 Yakobo ataona Rakele
mwana wa Labani, mlongo wa amayi ake, ali ndi nkhosa za Labani,
anapita nawugudubuza mwala uja nazimwetsa madzi nkhosa za amalume
akezo. 11 Kenaka Yakobo anapsompsona Rakele nayamba kulira mokweza.
12 Kenaka Yakobo anawuza Rakele kuti iye ndi mwana wa Rebeka, mlongo
wa abambo a Rakele uja. Choncho Rakele anathamanga nakawuza
abambo ake.
13 Labani atamva za Yakobo, mwana wa mlongo wake, anafulumira
kukakumana naye. Anamukupatira napsompsona, napita naye ku
nyumba kwake. Yakobo anafotokozera Labani zonse zinachitika. 14 Ndipo,
Labani anati kwa iye, “Iwe ndiwe ndithu fupa ndi mnofu wanga.”

*Yakobo Akwatira Leya ndi Rakele*

Yakobo anakhala ndi Labani mwezi umodzi. 15 Tsono Labani anawuza
Yakobo kuti, “Zoona iwe ndi ife ndi abale. Koma suyenera kundigwirira
ntchito popanda malipiro. Ndiwuze kuti malipiro ako azikhala wotani?”
16 Tsono Labani anali ndi ana aakazi awiri; dzina la wamkulu linali Leya,
ndipo dzina la wamng’ono linali Rakele. 17 Leya anali ndi maonekedwe
wofowoka koma Rakele anali wa maonekedwe wokongola kwambiri.

18 Yakobo anakonda Rakele ndipo anati, “Ndidzakugwirirani ntchito kwa
zaka zisanu ndi ziwiri chifukwa cha mwana wanu wamng’ono, Rakele.”
19 Labani anati, “Kuli bwino kuti ndimupereke kwa iwe ameneyu
kusiyana ndi munthu wina. Khala ndi ine kuno.” 20 Choncho Yakobo
anagwira ntchito zaka zisanu ndi ziwiri chifukwa cha Rakele. Koma kwa
iye zaka zonsezi zinakhala ngati masiku wochepa chifukwa anamukonda
Rakele.
21 Kenaka Yakobo anati kwa Labani, “Nthawi yanga ndakwanitsa,
ndipatseni mwana wanu kuti ndimukwatire.”
22 Pamenepo Labani anakonza phwando la ukwati, nayitana anthu onse
a pamalopo. 23 Koma pokwana usiku, Labani anatenga mwana wake
wamkazi Leya namupatsa Yakobo, ndipo Yakobo anagona naye. 24 Ndipo
Labani anapereka wantchito wake wamkazi Zilipa kwa Leya kuti akhale
wantchito wake.
25 Pakucha mmawa, Yakobo anaona kuti anagona ndi Leya. Choncho
Yakobo anafunsa Labani, “N’chiyani mwandichitirachi? Kodi ine sindi-
nakugwirireni ntchito chifukwa cha Rakele? Bwanji mwandinyenga?”
26 Labani anayankha, “Si mwambo wathu kuno kupereka wamng’ono
ku banja, wamkulu asanakwatiwe. 27 Yamba watsiriza sabata ya
chikondwerero cha ukwati wa Leya; kenaka ndidzakupatsanso Rakele.
Koma udzayenera kundigwirira ntchito zaka zisanu ndi ziwiri.”
28 Yakobo anachitadi momwemo. Anamaliza sabata ya chikondwerero
cha Leya, ndipo Labani anamupatsa Rakele kuti akhale mkazi wake.
29 Labani anapereka wantchito wake wamkazi Biliha kwa Rakele kuti
akhale wantchito wake. 30 Yakobo analowana ndi mkazi wake Rakele,
ndipo Yakobo anakonda Rakele kuposa Leya. Ndipo anamugwirira ntchito
Labani zaka zina zisanu ndi ziwiri chifukwa cha Rakele.

### *Ana a Yakobo*

31 Pamene Mulungu anaona kuti Yakobo sankamukonda Leya kwambiri,
Iye analola kuti Leya uja akhale ndi ana, ndi kuti Rakele akhale wosabala.
32 Leya anakhala ndi pathupi ndipo anabereka mwana wamwamuna. Ana-
mutcha Rubeni pakuti anati, “Yehova waona kusauka kwanga. Zoonadi,
mwamuna wanga adzandikonda tsopano.”
33 Anakhalanso ndi pathupi ndipo pamene anabereka mwana wamwa-
muna anati, “Yehova anamva kuti mwamuna wanga sakundikonda,
choncho wandipatsanso mwana winayu.” Ndipo anamutcha dzina lake
Simeoni.
34 Anatenganso pathupi kachitatu, ndipo pamene anabereka mwana
wamwamuna anati, “Pano pokha tidzaphatikana kwambiri ndi mwamuna
wanga, chifukwa ndamubalira ana aamuna atatu.” Kotero anamutcha
dzina lake Levi.
35 Anatenganso pathupi pena, ndipo pamene anabereka mwana
wamwamuna, iye anati, “Nthawi ino ndidzalemekeza Yehova.” Choncho
anamutcha Yuda. Kenaka analeka kubereka.

## 30

1 Rakele ataona kuti sakumuberekera Yakobo ana, anayamba kumuchi-
tira nsanje m’bale wake. Choncho anati kwa Yakobo, “Undipatse ana
kapena apo ayi ndingofa!”
2 Yakobo anapsera mtima Rakele ndipo nati, “Kodi ine ndalowa m’malo
mwa Mulungu amene wakulepheretsa iwe kukhala ndi ana?”

3 Pamenepo Rakele anati kwa Yakobo, "Mdzakazi wanga Biliha nayu.
Lowana naye kuti mwina n'kundibalira mwana, ndipo kudzera mwa iyeyu
nanenso n'kukhala ndi ana."
4 Ndipo anamupatsa Yakobo wantchito wake Biliha kuti alowane naye.
Choncho Yakobo analowana ndi Biliha, 5 ndipo Bilihayo anatenga pathupi
namubalira Yakobo mwana wamwamuna. 6 Pamenepo Rakele anati,
"Mulungu waweruza mondikomera mtima, wamva kupempha kwanga
ndipo wandipatsa mwana wa mwamuna." Choncho anamutcha Dani.
7 Biliha, wantchito wa Rakele, anatenganso pathupi nabalira Yakobo
mwana wa mwamuna wachiwiri. 8 Pamenepo Rakele anati, "Ndakhala
ndikulimbana kwambiri ndi m'bale wanga ndipo ndapambana." Choncho
anamutcha Nafutali.
9 Pamene Leya anaona kuti waleka kubereka ana, iye anatenga
wantchito wake Zilipa namupereka kwa Yakobo kuti alowane naye.
10 Zilipa, wantchito wa Leya, anaberekera Yakobo mwana wamwamuna.
11 Pamenepo Leya anati, "Mwayi wangawo!" Choncho anamutcha Gadi.
12 Zilipa, wantchito wa Leya anamubalira Yakobo mwana wa mwamuna
wachiwiri. 13 Pamenepo Leya anati, "Ndakondwa bwanji! Amayi
adzanditcha ine wokondwa." Choncho anamutcha Aseri.
14 Pa nthawi yokolola tirigu, Rubeni anapita ku munda ndipo anapezako
zipatso za mankhwala wobereketsa. Tsono anatengerako mayi wake Leya.
Rakele anati kwa Leya, "Chonde patseko mankhwala wakupezera mwana
wakowo."
15 Koma iye anati kwa Rakele, "Kodi sizinakukwanire kulanda mwa-
muna wanga? Ukuti utengenso mankhwala a mwana wangawa."
Iye anati, "Chabwino, agone ndi iwe usiku uno kuti tisinthane ndi
mankhwala a mwana wakowo."
16 Choncho pamene Yakobo ankabwera kuchokera ku munda madzulo,
Leya anapita kukakumana naye nati, "Lero mukagona ku nyumba chi-
fukwa ndakubwerekani ndi mankhwala wobereketsa a mwana wanga."
Choncho usiku umenewo Yakobo anakalowa kwa Leya.
17 Mulungu anamva pemphero la Leya ndipo anatenga pathupi nabalira
Yakobo mwana wa mwamuna wachisanu. 18 Pamenepo Leya anati,
"Mulungu wandipatsa mphotho chifukwa chopereka wantchito wanga
kwa mwamuna wanga." Choncho anamutcha Isakara.
19 Leya anatenganso pathupi nabalira Yakobo mwana wa mwamuna
wachisanu ndi chimodzi. 20 Pamenepo Leya anati, "Mulungu wandipatsa
mphatso yapamwamba. Tsopano mwamuna wanga adzandilemekeza
chifukwa ndamubalira ana aamuna asanu ndi mmodzi." Choncho
anamutcha Zebuloni.
21 Patapita nthawi Leya anabereka mwana wamkazi ndipo anamutcha
Dina.
22 Kenaka, Mulungu anakumbukira Rakele namva pemphero lake ndi
kulola kuti akhale ndi mwana. 23 Rakele anatenga pathupi nabala mwana
wamwamuna ndipo anati, "Mulungu wandichotsera manyazi anga." 24 Iye
anamutcha mwanayo Yosefe, ndipo anati, "Mulungu andipatsenso mwana
wina."

### *Nkhosa za Yakobo Zichuluka*

25 Rakele atabereka Yosefe, Yakobo anati kwa Labani, "Ndimasuleni kuti
ndizipita ku dziko la kwathu. 26 Patseni akazi anga ndi ana anga, amene
ndinakugwirirani ntchito, ndipo ndidzanyamuka ulendo. Inu mukudziwa
ntchito imene ndakugwirirani."

27 Koma Labani anati kwa iye, “Chonde, ngati mungandikomere mtima
musapite chifukwa ndadziwa kudzera mwa kuwombeza kwanga kuti
Yehova wandidalitsa chifukwa cha inu.” 28 Anapitiriza kunena kuti,
“Tchula malipiro ako ndipo ndidzakupatsa.”
29 Koma Yakobo anati kwa iye, “Inu mukudziwa mmene ine ndakug-
wirirani ntchito ndi mmene ziweto zanu zaswanira pamene ine ndi-
mazisamalira. 30 Poyamba munali nazo zochepa ine ndisanabwere, koma
tsopano zachuluka. Yehova wakudalitsani chifukwa cha ine. Ndi nthawi
tsopano kuti nane ndisamalire banja langa.”
31 Labani anafunsa, “Ndikupatse chiyani?”
Yakobo anayankha, “Musandipatse kanthu. Koma mungondichitira
izi ndipo ndidzapitiriza kusamalira nkhosa zanu ndi kuziyang’anira:
32 Mundilole ndiyendeyende pakati pa ziweto zanu lero ndi kuchot-
samo mwana wankhosa wamkazi aliyense wakuda, mbuzi iliyonse
yamathothomathotho ndi yamawangamawanga. Zimenezi ndiye zikhale
malipiro anga. 33 Ndipo chilungamo changa chidzaoneka m’tsogolo,
pamene inu mudzabwere kudzaona malipiro angawo. Ngati mudzapeza
mbuzi m’gulu langa imene si yamawangamawanga, kapena mwana
wankhosa wamkazi amene si wakuda ndiye kuti zimenezo zidzakhala kuti
ndinakuberani.”
34 Labani anati, “Ndavomera, zikhale monga mmene wayankhuliramu.”
35 Tsiku lomwelo Labani anachotsa atonde onse ndi mbuzi zazikazi
zonse zimene zinali ndi mawangamawanga kapena zamathothomathotho,
ndiponso zonse zabanga loyera. Anachotsa ana onse ankhosa aakazi
akuda, napereka ziweto zonsezi kwa ana ake aamuna kuti aziweta.
36 Kenaka Labani anayenda mtunda wa masiku atatu kutalikirana ndi
Yakobo koma Yakobo anapitiriza kuweta nkhosa zina zonse za Labani.
37 Tsono Yakobo anatenga nthambi zaziwisi za mitengo ya mkundi,
alimoni ndi puleni nazisenda kuchotsa makungwa ake mpaka mtengo
woyera wam’kati kuonekera. 38 Atatero anayika nthambi zija m’magome
omwera madzi molunjika ziweto zija kuti pakumwa madziwo ziweto
zazikazi ziziyang’ana nthambi zija popeza kuti pakumwa madzi ziweto
zija zinkakwerana. 39 Ndiye kuti nkhosa zija zinkatenga mawere
pakumwa madzi molunjika nthambi zija, ndipo zinkaswa ana a mawanga-
mawanga kapena a mathothomathotho. 40 Yakobo anayika padera ana
a ziweto zija. Koma ziweto zina anaziyika kuti ziyang’anane ndi
za Labani, zimene zinali za mawangamawanga ndi zakuda. Motero
anapeza ziweto zakezake, ndipo sanazisakanize ndi za Labani. 41 Yakobo
ankayika nthambi zija momwera madzi pamene ziweto zamphamvu
zazikazi zinkakweredwa pofuna kuti zitenge mawere pakumwa madzi
moyang’anana ndi nthambi zija. 42 Koma sankayika nthambizo pamene
ziweto zofowoka zazikazi zinkakweredwa pakumwa madzi. Choncho
ziweto zofowoka zonse zinakhala za Labani, ndi ziweto zamphamvu
zinakhala za Yakobo. 43 Mwa njira imeneyi, Yakobo analemera kwambiri
ndipo anali ndi ziweto zochuluka kwambiri, antchito aakazi ndi aamuna,
ngamira ndi abulu.

# 31

*Yakobo Athawa Labani*

1 Yakobo anamva zimene ana aamuna a Labani ankanena kuti, “Yakobo
watenga chilichonse cha abambo athu ndipo wapeza chuma chonsechi

pogwiritsa ntchito chuma cha abambo athu.” 2 Choncho Yakobo anaona
kuti Labani sankamuonetsanso nkhope yabwino monga kale.

3 Pamenepo Yehova anati kwa Yakobo, “Bwerera ku dziko la makolo ako
ndi kwa abale ako, ndipo Ine ndidzakhala nawe.”

4 Choncho Yakobo anatumiza mawu kukayitana Rakele ndi Leya kuti
abwere ku busa kumene ankaweta ziweto zake. 5 Iye anawawuza kuti,
“Abambo anu sakundionetsanso nkhope yabwino monga kale, koma
Mulungu wa makolo anga wakhala ali nane. 6 Inu mukudziwa kuti
ndagwirira ntchito abambo anu ndi mphamvu zanga zonse, 7 chonsecho
abambo anu akhala akundinyenga posintha malipiro anga kakhumi konse.
Komabe Mulungu sanalole kuti andichitire choyipa 8 Pamene abambo
anu anati, ‘Zamawangamawanga zidzakhala malipiro ako,’ ziweto zonse
zinaswa ana amawangamawanga; ndipo pamene anati, ‘Zamichocholozi
zidzakhala malipiro ako,’ ziweto zonse zinaswa ana a michocholozi.
9 Motero Mulungu walanda abambo anu ziweto zawo ndi kundipatsa.

10 “Pa nthawi imene ziweto zimatenga mawere ndinalota maloto, ndipo
ndinaona kuti atonde onse amene ankakwerawo anali amichocholozi,
amawangamawanga kapena amathothomathotho 11 Kutulo komweko, mn-
gelo wa Mulungu anati, ‘Yakobo.’ Ine ndinayankha, ‘Ee, Ambuye.’ 12 Ndipo
iye anati, ‘Tayang’ana ndipo taona kuti atonde onse okwerana ndi ziweto
ali amichocholozi, amawangamawanga kapena a mathothomathotho,
popeza ndaona zonse zimene Labani wakhala akukuchitira. 13 Ine ndine
Mulungu amene ndinadza kwa iwe pa Beteli paja. Beteli ndi kumalo kuja
kumene unayimika mwala ndi kuwudzoza mafuta, komanso kulumbira
kwa Ine. Tsopano choka m’dziko lino msanga ndi kubwerera ku dziko la
kwanu.’ ”

14 Pamenepo Rakele ndi Leya anayankha, “Kodi ngati ife tilinso ndi
gawo ngati cholowa pa chuma cha abambo athu? 15 Kodi abambo athu
samationa ife ngati alendo? Iwo anatigulitsa ndi kuwononga ndalama
zonse anazipeza pa ifezo. 16 Chuma chonse chimene Mulungu walanda
abambo athu, ndi chathu ndi ana athu. Tsono inu chitani zimene Mulungu
wakuwuzani.”

17 Pamenepo Yakobo anakonzeka nakweza ana ake ndi akazi ake pa
ngamira, 18 anakusa ziweto zake zonse patsogolo natenga katundu wake
yense amene anamupeza ku Padanaramu, ndipo ananyamuka kupita ku
Kanaani, ku dziko la abambo ake, Isake.

19 Labani atachoka pa khomo kupita kukameta nkhosa, m’mbuyomu
Rakele anaba timafano ta milungu ta abambo ake. 20 Komanso nthawi iyi
n’kuti Yakobo atamunamiza Labani Mwaramu posamuwuza zoona kuti
afuna kuthawa. 21 Choncho anathawa ndi zonse anali nazo. Ananyamuka
nawoloka mtsinje wa Yufurate kupita cha ku Giliyadi, dziko la mapiri.

### *Labani Alondola Yakobo*

22 Patapita masiku atatu, Labani anawuzidwa kuti Yakobo wathawa.
23 Pomwepo anatengana ndi abale ake namulondola Yakobo kwa masiku
asanu ndi awiri ndipo anakamupezera ku Giliyadi, dziko la mapiri.
24 Koma Mulungu anabwera kwa Labani, Mwaramu kutulo usiku nati kwa
iye, “Samala kuti usamuopseze Yakobo mwa njira iliyonse.”

25 Pamene Labani amamupeza Yakobo, n’kuti Yakobo atamanga matenti
ake ku mapiri a dziko la Giliyadi. Nayenso Labani ndi abale ake anamanga
matenti awo komweko. 26 Tsono Labani anati kwa Yakobo, “Kodi
ndakuchita chiyani kuti iwe undinamize ndi kutenga ana anga ngati anthu

ogwidwa ku nkhondo? 27 Chifukwa chiyani unandinamiza ndi kuthawa
mozemba wosandiwuza? Ukanandiwuza, bwezi titatsanzikana mwa
chisangalalo ndi kuyimba nyimbo ndi zisekese ndi azeze. 28 Sunandilole
kuti ndingopsompsona adzukulu anga ndi ana anga aakazi motsanzikana
nawo. Unachita zopusa. 29 Ndili nayo mphamvu yakukuchita choyipa;
koma usiku wapitawu, Mulungu wa abambo ako wandiwuza ine kuti,
'Usamuopseze Yakobo mwa njira iliyonse.' 30 Ndikudziwa kuti unachoka
chifukwa unapukwa kufuna kubwerera kwanu kwa abambo ako. Koma
n'chifukwa chiyani unaba milungu yanga?"

31 Yakobo anayankha Labani kuti, "Ine ndinkaopa chifukwa ndinka-
ganiza kuti mukhoza kundilanda anawa. 32 Koma mukapeza wina aliyense
ndi milungu yanu, ameneyo sakhala ndi moyo. Anthu onse akupenya,
lozani chilichonse chanu chimene chili ndi ine, ndipo ngati muchipeze
tengani. Koma Yakobo sankadziwa kuti Rakele anabadi milunguyo."

33 Choncho Labani analowadi mu tenti ya Yakobo, ya Leya ndi m'matenti
a adzakazi awiri aja, koma sanapeze kalikonse. Atatuluka mu tenti ya
Leya, analowa ya Rakele. 34 Koma Rakele anatengadi milungu ija ndi
kuyiika m'kati mwa chokhalira cha pa ngamira, iye n'kukhalapo. Choncho
Labani anafunafuna mu tenti monse koma wosapeza kanthu.

35 Rakele anati kwa abambo ake, "Pepanitu musandikwiyire mbuye
wanga chifukwa choti sinditha kuyimirira pamaso panu chifukwa ndili
kumwezi." Choncho Labani anafunafuna koma sanayipeze milungu ija.

36 Yakobo anapsa mtima nafunsa Labani mwaukali kuti, "Kodi ndalakwa
chiyani? Ndi tchimo lanji limene ndachita kuti muchite kundisaka
chonchi? 37 Chifukwa chiyani mwafunyulula katundu wanga? Ndipo
mwapeza chiyani cha inu pamenepa? Chimene mwapezapo chiyikeni
poyera pamaso pa abale anu ndi anga kuti atiweruze.

38 "Ndakhala nanu kwa zaka makumi awiri tsopano ndipo nkhosa ndi
mbuzi zanu sizinapoloze, kapena ine kudyapo nkhosa za m'khola mwanu.
39 Chiweto chikakhadzulidwa ndi chirombo, sindinkabwera nacho kwa
inu. Ineyo ndinkalipira. Inuyo munkandilipiritsa kalikonse kobedwa
masana kapena usiku. 40 Moyo wanga unali wotere: Dzuwa limanditentha
masana ndipo usiku ndimazunzika ndi kuzizira. Tulo sindimalipeza
konse. 41 Zinthu zinali chonchi kwa zaka makumi awiri zimene ndinali
m'nyumba mwanu. Ndinakugwirirani ntchito kwa zaka khumi ndi zinayi
chifukwa cha ana anu aakazi awiri ndipo zaka zina zisanu ndi chimodzi
chifukwa cha ziweto zanu, ndipo munandisinthira malipiro kakhumi
konse. 42 Akanapanda kukhala nane Mulungu wa abambo anga, Mulungu
wa Abrahamu ndi Mulungu amene Isake ankamuopa, mosakayika inu
mukanandichotsa chimanjamanja. Koma Mulungu waona zovuta zanga
ndi kulimbikira ntchito kwanga, ndipo usiku wapitawu anakudzudzulani."

43 Labani anayankha Yakobo nati, "Ana aakaziwa ndi anga, ana awo ndi
anganso. Ziwetozi ndi zanga. Chilichonse ukuona apa ndi changa. Koma
tsopano ndingachite chiyani ndi ana anga aakaziwa kapena ndi ana awo?
44 Tsono, tiye tichite pangano pakati pa iwe ndi ine, ndipo likhale mboni
pakati pathu."

45 Choncho Yakobo anayimiritsa mwala ngati chipilala. 46 Nati kwa abale
ake, "Tutani miyala ina." Choncho anawunjika miyalayo, ndipo anadya
chakudya atakhala pa mbali pa muluwo. 47 Labani anawutcha muluwo
Yegara-sahaduta, ndipo Yakobo anawutcha Galeeda.

48 Labani anati, “Mulu uwu ndi mboni pakati pa inu ndi ine lero.”
Ndi chifukwa chake unatchedwa Galeeda. 49 Unatchedwanso Mizipa,
chifukwa iye anati, “Yehova aonetsetsa kuti palibe mmodzi mwa ife
adzaswe panganoli ngakhale titatalikirana. 50 Ngati ukazunza ana anga
kapena kukwatira akazi enanso, ngakhale kuti palibe wina amene ali nafe
pano, koma kumbukira kuti Mulungu ndiye mboni pakati pathu.”
51 Labani anatinso kwa Yakobo, “Taona pano pali miyala ndi chipilala
chimene ndayimika pakati pa iwe ndi ine. 52 Mulu wa miyala uwu
ndi chipilalachi ndi mboni. Ine sindidzadutsa mulu wa miyalawu
kudzalimbana ndi iwe. Iwenso usadzadutse mulu wa miyalawu kudza-
limbana nane. 53 Mulungu wa Abrahamu ndi Mulungu wa Nahori ndiye
adzatiweruze.”
Choncho Yakobo analumbira m’dzina la Mulungu amene Isake, abambo
ake ankamuopa. 54 Yakobo anapereka nsembe pa phiri paja, ndipo
anayitana abale ake kuti adzadye chakudya. Atadya chakudya anagona
pa phiri pomwepo.
55 Mmamawa wake, Labani anapsompsona zidzukulu zake ndi ana ake
nawadalitsa. Kenaka ananyamuka kubwerera ku mudzi.

# 32

### *Yakobo Akonzekera Kukumana ndi Esau*

1 Nayenso Yakobo analowera njira yake, ndipo angelo a Mulungu
anakumana naye. 2 Pamene Yakobo anawaona anati, “Ili ndi gulu la
Mulungu.” Choncho anawatcha malowo Mahanaimu.
3 Yakobo anatumiza amithenga ake kwa m’bale wake Esau ku dera la
Seiri, dziko la Edomu. 4 Anawalangiza kuti, “Zimene mukanene ndi izi
kwa mbuye wanga Esau: ‘Mtumiki wanu Yakobo akuti, Ine ndakhala ndi
kukhala ndi Labani mpaka tsopano. 5 Ndili ndi ng’ombe, abulu, nkhosa
ndi mbuzi, antchito aamuna ndi aakazi. Tsopano ndikutumiza mawu
amenewa kwa mbuye wanga, kuti mundikomere mtima.’ ”
6 Pamene amithenga aja anabwerera kwa Yakobo, anati, “Tinapita kwa
m’bale wanu Esau, ndipo tsopano iye akubwera kudzakumana nanu. Ali
ndi anthu 400.”
7 Yakobo anali ndi mantha ndi nkhawa yayikulu kwambiri. Tsono
anagawa anthu onse amene anali naye, ndiponso nkhosa, mbuzi, ng’ombe
ndi ngamira m’magulu awiri. 8 M’maganizo ake iye ankanena kuti, “Ngati
Esau atabwera ndi kuthira nkhondo gulu limodzi, gulu lina lotsalalo
likhoza kupulumuka.”
9 Pamenepo Yakobo anapemphera, “Haa, Mulungu wa kholo langa
Abrahamu, Mulungu wa abambo anga Isake, Aa Yehova amene munati
kwa ine, ‘Bwerera ku dziko la kwanu ndi kwa abale ako, ndipo ndidza-
kuchitira zabwino.’ 10 Ine siwoyenera kulandira kukoma mtima kwanu
ndi kukhulupirika kwanu kumene mwaonetsa wantchito wanu. Ndinali
ndi ndodo yokha pamene ndinawoloka Yorodani uyu koma tsopano ndili
ndi magulu awiri. 11 Ndipulumutseni m’dzanja la m’bale wanga Esau,
popeza ndikuopa kuti mwina akubwera kudzandithira nkhondo pamodzi
ndi akazi ndi ana omwe. 12 Paja Inu munandilonjeza kuti simudzalephera
kundichitira zabwino ndi kuti zidzukulu zanga zidzakhala zosawerengeka
ngati mchenga wa ku nyanja.”
13 Iye anagona pomwepo usiku umenewo. Pambuyo pake anasankhula
pa chuma chimene anali nacho zinthu izi ngati mphatso za Esau, m’bale

wake: 14 Anasankhula mbuzi zazikazi 200 ndi atonde makumi awiri,
nkhosa zazikazi 200 ndi nkhosa zazimuna makumi awiri, 15 ngamira za
mkaka 30 ndi ana awo, ng'ombe zazikazi 40 ndi zazimuna khumi, ndipo
abulu aakazi makumi awiri ndi abulu aamuna khumi. 16 Iye anazipereka
kwa antchito ake kuti azikuse, gulu lililonse pa lokha, ndipo anati kwa
antchito akewo, "Tsogolani ndipo muonetsetse kuti pali mpata pakati pa
gulu ndi gulu linzake."

17 Anawuza mnyamata wa gulu loyamba kuti, "Ngati ukumana naye
m'bale wanga Esau nakufunsa kuti, 'Ndinu antchito a yani, ndipo
mukupita kuti? Nanga ziweto zonse zili patsogolo pakozi ndi za yani?'
18 Pamenepo ukayankhe kuti, 'Zimenezi ndi za wantchito wanu, Yakobo,
ndipo wazipereka kwa inu, Esau, mbuye wake ngati mphatso. Mtumiki
wanuyu akubwera m'mbuyo mwathumu.' "

19 Anawuza mawu omwewo kwa wachiwiri, wachitatu ndi ena
onse amene ankayenda motsogoza ziwetozo kuti, "Inunso munene
zomwezo kwa Esau mukakumana naye. 20 Muzikanena kuti, 'Wantchito
wanu Yakobo akubwera m'mbuyo mwathumu.' " Popeza anaganiza kuti,
"Ndidzamutsitsa mtima ndi mphatso ndazitsogozazi. Apo tsono ndikadza-
kumana naye, mwina adzandilandira bwino." 21 Choncho mphatso za
Yakobo zinatsogola, koma iye mwini anagona pa msasa pomwepo usiku
umenewo.

### *Yakobo Alimbana ndi Mulungu*

22 Usiku umenewo Yakobo anauka natenga akazi ake awiri, antchito
ake awiri ndi ana ake aamuna khumi ndi mmodzi nawoloka pa dooko la
mtsinje wa Yaboki. 23 Atatha kuwawolotsa pa mtsinjewo anawolotsanso
katundu wake yense. 24 Tsono Yakobo anatsala yekha. Tsono munthu
wina anadzalimbana naye mpaka m'mbandakucha. 25 Pamene munthuyo
anaona kuti sangathe kumugonjetsa, anakhudza nyung'unyu ya pa
ntchafu ya Yakobo ndipo inaguluka polimbanapo. 26 Kenaka munthuyo
anati, "Ndisiye ndizipita, popeza kunja kukucha."

Koma Yakobo anayankha, "Sindikulolani kupita pokhapokha mutandi-
dalitsa."

27 Munthu uja anamufunsa Yakobo kuti, "Kodi dzina lako ndiwe yani?"

Iye anayankha, "Ndine Yakobo."

28 Pamenepo munthuyo anati, "Dzina lako silidzakhalanso Yakobo koma
Israeli, chifukwa walimbana ndi Mulungu ndi anthu ndipo wapambana."

29 Yakobo anati, "Chonde, uzeni dzina lanu."

Koma munthuyo anati, "Chifukwa chiyani ukundifunsa dzina?" Kenaka
anamudalitsa pomwepo.

30 Choncho Yakobo anawatcha malowo Penueli, popeza anati, "Ndinao-
nana ndi Mulungu maso ndi maso koma sindinafe."

31 Dzuwa linamutulukira Yakobo pamene amachoka pa Penueli.
Tsono ankayenda chotsimphina chifukwa cha nyung'unyu yake ija.
32 N'chifukwa chake mpaka lero Aisraeli sadya nyama ya pa nyung'unyu
chifukwa Yakobo anakhudzidwa pa nyung'unyu.

## 33

### *Yakobo Akumana ndi Esau*

1 Yakobo atakweza maso ake anaona Esau akubwera ndi anthu ake
400. Choncho ana ake anawagawira Leya, Rakele ndi antchito awiri aja.

2 Anayika antchito ndi ana awo patsogolo, kenaka n'kubwera Leya ndi
ana ake, ndipo pambuyo pawo Rakele ndi Yosefe. 3 Iye mwini anakhala
patsogolo nawerama mpaka kukhudza pansi kasanu ndi kawiri pamene
amayandikira m'bale wake.

4 Koma Esau anathamanga kukakumana ndi Yakobo ndipo anamuku-
patira namupsompsona. Onse awiri ankangolira. 5 Kenaka Esau ataona
amayi ndi ana awo anamufunsa Yakobo kuti, "Kodi anthu amene uli
nawowa ndi a ndani?"

Yakobo anayankha kuti, "Awa ndi ana amene Mulungu, mwa kukoma
mtima kwake, wapereka kwa mtumiki wanune."

6 Tsono antchito aja anayandikira naweramitsa mitu pansi. 7 Kenaka,
Leya ndi ana ake anabwera. Nawonso anaweramitsa mitu pansi. Potsiriza
pa onse anabwera Yosefe ndi Rakele naweramitsanso mitu yawo pansi.

8 Esau anafunsa kuti, "Kodi gulu la ziweto ndakumana nalo lija ndi
layani?"

Yakobo anayankha nati, "Mbuye wanga, gulu lija ndi lanu kuti
mundikomere mtima."

9 Koma Esau anati, "M'bale wanga, ine ndili nazo kale zambiri. Zinthu
zakozi sunga."

10 Yakobo anati, "Chonde musatero. Ngati mwandikomera mtima,
landirani mphatso yangayi kuchokera kwa ine. Pakuti ndi mmene
mwandirandira bwinomu, ine ndikamaona nkhope yanu ndikuchita
ngati ndikuona nkhope ya Mulungu. 11 Chonde, landirani mphatso
imene ndakutengeraniyi, popeza Mulungu wandikomera mtima kwambiri
moti ndili ndi zonse zimene ndizifuna." Ndipo popeza kuti Yakobo
anamuwumiriza, Esau analandira.

12 Ndipo Esau anati, "Tiyeni tizipita; nditsagana nanu."

13 Koma Yakobo anati kwa iye, "Mbuye wanga, inu mudziwa kuti anawa
ndi a nthete ndiponso ndiyenera kusamalira nkhosa ndi ng'ombe zimene
zikuyamwitsa ana awo. Ngati ndizimenya kuti zifulumire, tsiku limodzi
lokha nyamazo zidzafa. 14 Choncho, mbuye wanga lolani kuti mutsogole.
Ine ndiziyenda pang'onopang'ono pambuyo pa ziwetozi ndi anawa mpaka
ndikafika ku Seiri."

15 Esau anati, "Ndiye bwanji ndikusiyireko ena mwa anthu anga."

Koma Yakobo anati, "Koma muchitiranji zimenezi? Chachikulu n'kuti
mwandilandira bwino, mbuye wanga."

16 Choncho tsiku limenelo Esau anayamba ulendo wobwerera ku Seiri.
17 Komabe Yakobo anapita ku Sukoti. Kumeneko anamanga nyumba yake
ndi makola a ziweto zake. N'chifukwa chake malowa amatchedwa Sukoti.

18 Mmene ankabwerera kuchokera ku Padanaramu, Yakobo anafika ku
Salemu, mzinda wa Sekemu ku Kanaani. Anamanga msasa pamalopo
moyang'anana ndi mzindawo. 19 Malo amenewo anagula kwa zidzukulu
za Hamori, abambo a Sekemu ndi ndalama 100 zasiliva. 20 Pamalopo
anamanganso guwa lansembe, nalitcha Eli Elohe Israeli.

# 34

*Dina ndi Sekemu*

1 Tsopano Dina, mwana amene Leya anaberekera Yakobo, anapita
kukacheza ndi akazi ena a m'dzikolo. 2 Pamene Sekemu mwana wa
Hamori Mhivi, mfumu ya deralo, anamuona, anamugwirira. 3 Koma
Sekemu anamukondadi namwali uja, Dina, mwana wa Yakobo motero

kuti anamuyankhula mawu womutonthoza. 4 Choncho Sekemu anati
kwa abambo ake Hamori, “Mundipezere mtsikana uyu kuti akhale mkazi
wanga.”
5 Yakobo anamva kuti mwana wake Dina wagwiriridwa, koma sana-
chitepo kanthu msanga kudikira mpaka ana ake amuna omwe anali ku
busa atabwerako.
6 Kenaka Hamori, abambo a Sekemu, anapita kukakambirana ndi
Yakobo. 7 Pa nthawi iyi n’kuti ana a Yakobo atabwererako ku busa kuja.
Iwo atangomva zimene zinachitika, anawawidwa mtima. Iwo anapsa
mtima kwambiri kuti Sekemu n’kuchita chonyansa choterechi mu dziko
la Israeli, kumugwirira Dina, mwana wa Yakobo.
8 Koma Hamori anawawuza kuti, “Mwana wanga Sekemu wamukonda
kwambiri mwana wanu. Chonde muloleni kuti akhale mkazi wake.
9 Tiyeni tichite mgwirizano wa ukwati kuti ife tidzikwatira ana anu ndi
inu mudzikwatira ana athu. 10 Khazikikani pakati pathu. Mukhoza kupeza
malo wokhala kulikonse kumene mufuna. Mukhozanso kuchita malonda
momasuka ndi kupeza chuma.”
11 Pamenepo Sekemu anati kwa abambo ndi alongo ake a Dina, “Inu
mundikomere mtima, ndipo ndidzakupatsani chilichonse munganene.
12 Tchulani mtengo wamalowolo umene ndiyenera kupereka, ndipo
ndipereka. Ndidzakupatsani chilichonse chimene mukufuna malingana
inu mukandipatsa namwaliyu kuti ndimukwatire.”
13 Ana a Yakobo anayankha Sekemu ndi abambo ake, Hamori
mwachinyengo chifukwa mlongo wawo, Dina anali atayipitsidwa. 14 Iwo
anati, “Sitingachite zimenezo, kupereka mlongo wathu kwa munthu
wosachita mdulidwe. Chimenecho ndi chinthu cha manyazi kwa ife.
15 Tikuvomerani pokhapokha mutakhala ngati ife, mutachita mdulidwe
ana anu onse aamuna. 16 Kenaka tidzakulolani kuti mukwatire ana
athu, ifenso tizikwatira ana anu. Choncho tidzakhala pakati panu ndipo
tidzakhala anthu amodzi. 17 Koma ngati simuvomereza kuchita mdulidwe
titenga mlongo wathu ndi kupita.”
18 Mawu amenewa anakondweretsa Hamori ndi mwana wake Sekemu.
19 Mnyamata uja amene anali wolemekezeka kwambiri pa banja lake
lonse, sanachedwe kuchita mdulidwe popeza anamukonda kwambiri
mwana wa Yakobo. 20 Choncho Hamori ndi mwana wake Sekemu
anapita ku chipata cha mzinda wawo kukayankhula ndi anthu a mu
mzindawo. 21 Iwo anati, “Anthu awa ndi a mtendere. Aloleni kuti
akhale m’dziko mwathu muno nachitamo malonda. Dzikoli lili ndi malo
ambiri woti iwo n’kukhalamo. Tingathe kukwatira ana awo aakazi ndipo
angathe kukwatira ana athu aakazi. 22 Komatu anthuwa adzavomereza
kukhala amodzi a ife pokhapokha ngati amuna onse pakati pathu atachita
mdulidwe monga alili iwo. 23 Tikatero, ndiye kuti ziweto zawo zonsezi,
katundu wawo yenseyu ndi ziweto zawo zina zonsezi zidzakhala zathu.
Choncho tiyeni tiwavomereze ndipo adzakhazikika pakati pathu.”
24 Amuna onse amene anatuluka ku chipata cha mzinda anavomerezana
ndi Hamori ndi mwana wake Sekemu, ndipo aliyense wamwamuna mu
mzindamo anachita mdulidwe.
25 Patapita masiku atatu, amuna onse akumvabe ululu wa kuchita
mdulidwe uja, ana awiri a Yakobo, Simeoni ndi Levi, alongo ake a Dina,
anatenga malupanga ndi kulowa mu mzindawo mwakachetechete napha
amuna onse. 26 Anapha Hamori ndi Sekemu. Anakatenga Dina ku nyumba
kwa Sekemu nanyamuka. 27 Ana a Yakobo anafika kwa anthu ophedwawo

ndi kututa katundu mu mzindawo chifukwa anagwiririra mlongo wawo.
28 Analanda nkhosa zawo, ng'ombe zawo, abulu awo ndi china chilichonse
chawo mu mzindamo pamodzi ndi za ku minda. 29 Anawatengera chuma
chawo chonse, akazi ndi ana awo, pamodzi ndi zonse zimene zinapezeka
m'nyumba zawo. Zonsezi zinayesedwa ngati zolandidwa ku nkhondo.

30 Pamenepo Yakobo anati kwa Simeoni ndi Levi, "Mwandiputira
mavuto, ndi kundiyipitsira dzina pakati pa anthu a m'dziko lino, Akanaani
ndi Aperezi. Ife ndife owerengeka, ndipo atati aphatikizane kudzandithira
nkhondo, ndiye kuti ine ndi banja langa tidzawonongeka."

31 Koma iwo anayankha kuti, "Pepani, nanga achite kumusandutsa
mlongo wathu ngati mkazi wachiwerewere?"

# 35

*Yakobo Abwerera ku Beteli*

1 Tsono Mulungu anati kwa Yakobo, "Nyamuka uchoke kuno kupita ku
Beteli. Kumeneko ukamange guwa lansembe la Mulungu amene anadza
kwa iwe pamene umathawa Esau, m'bale wako."

2 Choncho Yakobo anawuza a pa banja pake ndi onse amene anali naye
kuti, "Chotsani milungu yachilendo imene muli nayo, ndipo mudziyeretse
nokha ndi kusintha zovala zanu. 3 Tiyeni tinyamuke kuchoka kuno kupita
ku Beteli. Kumeneko ndikamumangira guwa lansembe Mulungu amene
anandithandiza pa nthawi za masautso anga, komanso amene wakhala
nane m'mayendedwe anga onse." 4 Choncho anamupatsa Yakobo milungu
yachilendo yonse imene anali nayo pamodzi ndi ndolo. Iye anazikwirira
pansi pa mtengo wa thundu ku Sekemu. 5 Pamenepo ananyamuka, ndipo
mtima woopa Mulungu unagwera anthu onse a m'mizinda yozungulira,
kotero kuti palibe aliyense amene anatsatira banja la Yakobo.

6 Yakobo ndi anthu onse anali naye aja anafika ku Luzi (ku Beteli) mu
dziko la Kanaani. 7 Kumeneko anamanga guwa lansembe nalitcha Eli
Beteli, chifukwa kunali kumeneko kumene Mulungu anadziwulula yekha
kwa Yakobo pamene ankathawa m'bale wake.

8 Debora mlezi wa Rakele anamwalira komweko nayikidwa m'manda
pansi pa mtengo wa thundu cha kumunsi kwa Beteli. Choncho
panatchedwa Aloni-Bakuti (mtengo wamaliro).

9 Yakobo atabwera kuchokera ku Padanaramu, Mulungu anabweranso
kwa iye namudalitsa. 10 Mulungu anati kwa iye, "Dzina lako ndiwe Yakobo,
koma sudzatchedwanso Yakobo; koma udzatchedwa Israeli." Choncho
anamutcha iye Israeli.

11 Ndipo Mulungu anati kwa iye, "Ine ndine Mulungu Wamphamvu-
zonse; berekanani ndi kuchulukana. Mtundu wa anthu, inde, mitundu
yambiri ya anthu idzatuluka mwa iwe, ndipo ena mwa zidzukulu zako
adzakhala mafumu. 12 Dziko limene ndinapereka kwa Abrahamu ndi
Isake ndiliperekanso kwa iwe. Lidzakhala lako ndi la zidzukulu zako."
13 Kenaka Mulungu anamusiya Yakobo.

14 Yakobo anayika mwala wachikumbutso pa malo pamene Mulungu
anayankhula naye paja. Iye anathirapo nsembe yachakumwa ndi
yamafuta. 15 Yakobo anawatcha malo amene Mulungu anayankhula naye
aja kuti Beteli.

*Imfa ya Isake ndi Rakele*

16 Kenaka anachoka ku Beteli. Koma ali pafupi kufika ku Efurata
nthawi yakuti Rakele aone mwana inakwana. Iye anavutika pobereka.
17 Akanali chivutikire choncho, mzamba anamulimbikitsa nati, “Usaope
pakuti ubala mwana wina wamwamuna.” 18 Tsono pamene Rakele
ankapuma wefuwefu (popeza ankamwalira) iye anatcha mwana uja kuti
Beni-Oni. Koma abambo ake anamutcha kuti Benjamini.

19 Choncho Rakele anamwalira ndipo anayikidwa pa njira yopita ku
Efurata (Kumeneko ndiye ku Betelehemu). 20 Pa manda ake, Yakobo
anayimika mwala wachikumbutso wa pa manda ndipo ulipobe mpaka
lero.

21 Israeli (Yakobo) anasunthanso nakamanga tenti yake kupitirira nsanja
ya Ederi. 22 Israeli akanali m'derali, Rubeni anapita nakagonana ndi
Biliha, mdzakazi wa abambo ake. Yakobo uja anazimva zimenezi.

Yakobo anali ndi ana aamuna khumi ndi awiri:

23 Ana a Leya ndi awa:
Rubeni anali mwana woyamba wa Yakobo,
Simeoni, Levi, Yuda, Isakara, ndi Zebuloni.

24 Ana a Rakele ndi awa:
Yosefe ndi Benjamini.

25 Ana a Biliha, wantchito wa Rakele ndi awa:
Dani ndi Nafutali.

26 Ana a Zilipa wantchito wa Leya ndi awa:
Gadi ndi Aseri.

Awa ndiwo ana a Yakobo amene anabadwira ku Padanaramu.

27 Yakobo anafika ku mudzi kwa abambo ake Isake ku Mamre, (kumene
kunkatchedwa ku Kiriyati-Ariba kapenanso Hebroni) kumene Abrahamu
ndi Isake anakhalako kale. 28 Isake anakhala ndi moyo zaka 180.
29 Anamwalira ali wokalamba kwambiri ndipo anakakhala ndi anthu a
mtundu wake. Ndipo ana ake Esau ndi Yakobo anamuyika m'manda.

# 36

*Zidzukulu za Esau*

1 Nazi zidzukulu za Esau amene ankatchedwanso Edomu:

2 Esau anakwatira akazi atatu a ku Kanaani. Iwowa ndiwo Ada
mwana wa Eloni Mhiti; Oholibama mwana wa Ana amene anali mwana
wa Zibeoni Mhivi 3 ndi Basemati mwana wa Ismaeli, amenenso anali
mlongo wa Nabayoti.

4 Ada anaberekera Esau, Elifazi; Basemati anabereka Reueli; 5 ndipo
Oholibama anabereka Yeusi, Yolamu ndi Kora. Amenewa anali ana a
Esau amene anabadwira ku Kanaani.

6 Esau anatenga akazi ake, ana ake aamuna ndi aakazi ndi ena onse a
pa banja pake. Anatenganso ziweto zake ndi ziweto zake zonse pamodzi
ndi katundu wake yense amene anamupata ku Kanaani, ndipo anachoka
ku dziko la Kanaani kupatukana ndi m'bale wake Yakobo. 7 Iwo anatero
chifukwa dziko limene ankakhalamo silikanakwanira awiriwo. Iwowa
anali ndi ziweto zochuluka motero kuti sakanatha kukhala pamodzi.
8 Choncho Esau (amene ndi Edomu) anakakhazikika ku dziko la mapiri
ku Seiri.

9 Nazi zidzukulu za Esau, kholo la Aedomu amene ankakhala ku Seiri.

10 Awa ndi mayina a ana aamuna a Esau:
Elifazi, mwana wa Ada, mkazi wa Esau, ndi Reueli, mwana wamwamuna wa Basemati, mkazi wa Esau.
11 Awa ndi mayina a ana a Elifazi:
Temani, Omari, Zefo, Gatamu ndi Kenazi.
12 Timna anali mzikazi wa Elifazi, mwana wa Esau. Iyeyo anaberekera Elifazi mwana dzina lake Amaleki. Amenewa ndiwo zidzukulu za Ada, mkazi wa Esau.
13 Awa ndi ana a Reueli:
Nahati, Zera, Sama ndi Miza. Amenewa ndi ana a Basemati, mkazi wa Esau.
14 Ana aamuna a Oholibama, mkazi wa Esau, mwana wa Ana ndi mdzukulu wa Zebeoni ndi awa:
Yeusi, Yolamu ndi Kora.

15 Nawa mafumu a zidzukulu za Esau:
Mwa ana a Elifazi, mwana woyamba wa Esau panali mafumu awa:
Temani, Omari, Zefo, ndi Kenazi, 16 Kora, Gatamu, ndi Amaleki. Awa anali mafumu mwa ana a Elifazi ku Edomu ndipo onsewa anali zidzukulu za Ada.
17 Mwa ana a Reueli, mwana wa Esau munali mafumu awa:
Nahati, Zera, Sama ndi Miza. Awa anali mafumu mwa ana a Reueli ku Edomu. Iwowa anali zidzukulu za Basemati mkazi wa Esau.
18 Mwa ana a Oholibama, mkazi wa Esau munali mafumu awa:
Yeusi, Yolamu, ndi Kora. Amenewa anali mafumu mwa ana a mkazi wa Esau, Oholibama, mwana wa Ana.
19 Amenewa ndiwo zidzukulu za Esau (amene ndi Edomu) ndiponso
mafumu awo.

20 Awa ndi ana a Seiri Mhori, amene ankakhala m'dzikomo:
Lotani, Sobala, Zibeoni, Ana, 21 Disoni, Ezeri ndi Disani. Amenewa ndiwo ana a Seiri a ku Edomu ndipo analinso mafumu a Ahori.
22 Ana aamuna a Lotani anali awa:
Hori ndi Homamu. Timna anali mlongo wake wa Lotani.
23 Ana aamuna a Sobala anali awa:
Alivani, Manahati, Ebala, Sefo ndi Onamu.
24 Ana aamuna a Zibeoni anali awa:
Ayiwa ndi Ana. Uyu ndi Ana amene anapeza akasupe a madzi amoto m'chipululu pamene ankadyetsa abulu abambo wake Zibeoni.
25 Ana a Ana anali:
Disoni ndi Oholibama mwana wake wamkazi.
26 Ana aamuna a Disoni anali awa:
Hemudani, Esibani, Itirani ndi Kerani.
27 Ana aamuna a Ezeri anali awa:
Bilihani, Zaavani ndi Akani.
28 Ana aamuna a Disani anali awa:
Uzi ndi Arani.
29 Mafumu a Ahori anali awa:
Lotani, Sobala, Zibeoni, Ana, 30 Disoni, Ezeri ndi Disani. Amenewa ndiwo mafumu a Ahori, monga mwa mafuko awo, m'dziko la Seiri.

### *Mafumu a ku Edomu*

31 Awa ndi mafumu amene ankalamulira dziko la Edomu, mfumu
iliyonse ya Israeli isanayambe kulamulira kumeneko:

32 Bela mwana wa Beori anakhala mfumu ya ku Edomu. Mzinda wake
ankawutcha Dinihaba.
33 Bela atamwalira, Yobabu mwana wa Zera wochokera ku Bozira
analowa ufumu m'malo mwake.
34 Atafa Yobabu, Husamu wochokera ku dziko la Atemani, analowa
m'malo mwake ngati mfumu.
35 Husamu atamwalira, Hadadi mwana wa Bedadi, amene anagonjetsa
Amidiyani m'dziko la Mowabu, analowa ufumu m'malo mwake.
Mzinda wake unkatchedwa Aviti.
36 Hadadi atamwalira, Samila wochokera ku Masireka, analowa ufumu
m'malo mwake.
37 Samila atamwalira, Sauli wochokera ku Rehoboti wa ku Mtsinje,
analowa ufumu m'malo mwake.
38 Sauli atamwalira, Baala-Hanani, mwana wa Akibori analowa ufumu
m'malo mwake.
39 Pamene Baala-Hanani mwana wa Akibori anamwalira, Hadari
analowa ufumu m'malo mwake. Mzinda wake unkatchedwa Pau,
ndipo dzina la mkazi wake linali Mehatabeli, mwana wamkazi wa
Matiredi, mwana wamkazi wa Me-Zahabu.

40 Mayina a mafumu ochokera mwa zidzukulu za Esau malingana ndi
mafuko awo ndi malo a fuko lililonse anali awa:
Timna, Aliva, Yeteti, 41 Oholibama, Ela, Pinoni, 42 Kenazi, Temani,
Mibezari, 43 Magidieli ndi Iramu. Awa anali mafumu a ku Edomu
molingana ndi malo awo okhala m'dzikomo.

Umenewu ndi mndandanda wa m'bado wa Esau, kholo la Aedomu.

# 37

*Maloto a Yosefe*

1 Yakobo ankakhala m'dziko la Kanaani kumene abambo ake ankakhala.

2 Mbiri ya banja la Yakobo ndi iyi:

Yosefe, mnyamata wa zaka 17 ankaweta nkhosa ndi abale ake, pamodzi
ndi ana a Biliha ndi Zilipa, akazi a abambo ake. Tsono Yosefe ankabwera
kudzawuza abambo ake zoyipa za abale ake.
3 Tsono Israeli ankakonda Yosefe koposa ana ake ena onse, chifukwa
anali mwana wobadwa muukalamba wake. Ndipo anamusokera mkanjo
wa manja aatali. 4 Pamene abale ake anaona kuti abambo awo
ankakonda Yosefe kuposa aliyense wa iwo, anayamba kumuda Yosefe
ndipo sankayankhula naye zamtendere.
5 Tsiku lina Yosefe analota maloto ndipo pamene anawuza abale ake za
malotowo, iwo anawonjeza kumuda. 6 Iye anawawuza kuti, "Tamvani
maloto amene ndinalota: 7 Ife timamanga mitolo ya tirigu ku munda
ndipo mwadzidzidzi mtolo wanga unayimirira chilili, pamene mitolo yanu
inazungulira mtolo wangawo n'kumawugwadira."
8 Abale ake aja anamufunsa nati, "Kodi ukuyesa kuti ungakhale mfumu
yathu? Ungadzatilamuliredi iweyo?" Ndipo anamuda kuposa kale
chifukwa cha maloto ake ndi zimene ankakonda kunena kwa abambo awo.
9 Tsiku lina analotanso maloto ena, ndipo anafotokozera abale ake za
malotowo. Iye anati, "Tamverani, ndinalotanso maloto ena. Ulendo uno

dzuwa ndi mwezi pamodzi ndi nyenyezi khumi ndi imodzi zimandig-
wadira.”
10 Atawuza abambo ake ndi abale ake malotowa, abambo ake ana-
mukalipira nati, “Ndi maloto anji umalotawa? Kodi uganiza kuti ine,
amayi ako pamodzi ndi abale ako onsewa tingadzabwere kudzakug-
wandira iwe?” 11 Abale ake anamuchitira nsanje, koma abambo ake
anasunga nkhaniyi mu mtima.

### *Yosefe Agulitsidwa ndi Abale Ake*

12 Tsono abale ake anapita kukadyetsa ziweto za abambo awo ku
Sekemu, 13 ndipo Israeli anati kwa Yosefe, “Tsono, ndikufuna kukutuma
kwa abale ako.”

Iye anayankha nati, “Chabwino.”

14 Choncho anati kwa iye, “Pita ukaone ngati abale ako ali bwino.
Ukaonenso nkhosa ngati zili bwino. Kenaka ubwere udzandiwuze.”
Choncho Israeli anatuma Yosefe kuchokera ku chigwa cha Hebroni.

Yosefe atafika ku Sekemu, 15 munthu wina anamupeza akungozunguli-
razungulira m’munda ndipo anamufunsa, “Ukufunafuna chiyani?”

16 Iye anayankha, “Ndikufuna abale anga. Mungandiwuze kumene
akudyetsa ziweto zawo?”

17 Munthuyo anayankha nati, “Anasamukako kuno. Ndinawamva akuti,
‘Tiyeni tipite ku Dotani.’ ”

Choncho Yosefe analondola abale ake ndipo anakawapeza ku Dotani.
18 Abale ake aja anamuonera patali. Ndipo asanafike n’komwe kumene
kunali iwo kuja, anayamba kale kumupangira chiwembu choti amuphe.

19 Iwo anawuzana nati, “Uyo akubwera apo wamaloto uja. 20 Tsono
tiyeni timuphe ndi kuponya thupi lake mu chimodzi mwa zitsime izi
ndipo tidzati anadyedwa ndi nyama zakuthengo zolusa. Tsono timuonera
zomwe ziti zichitike ndi maloto ake aja.”

21 Koma Rubeni atamva izi, anapulumutsa Yosefe. Iye anati kwa abale
ake, “Ayi, tisamuphe, 22 tisakhetse magazi. Tiyeni timuponye m’chitsime
ku chipululu konkuno. Koma tisamuvulaze n’komwe. Rubeni ananena
zonsezi kuti apulumutse Yosefe ndi kuti pambuyo pake akamupereke kwa
abambo awo.”

23 Choncho Yosefe atafika kwa abale ake, iwo anamuvula mkanjo wake
wamanja aatali uja umene anavala 24 ndipo anamutenga namuponya
m’chitsime chopanda madzi komanso mopanda chilichonse.

25 Atakhala pansi kuti adye chakudya, anatukula maso naona gulu la
Aismaeli akubwera kuchokera ku Giliyadi. Ngamira zawo zinanyamula zo-
nunkhiritsa bwino zakudya zamitundumitundu, ndipo zimenezi ankapita
nazo ku Igupto.

26 Yuda anafunsa abale ake nati, “Kodi tidzapindula chiyani tikapha
m’bale wathuyu ndi kuphimbitsa magazi ake? 27 Bwanji timugulitse kwa
Aismaeliwa, koma ife tisamuchite kanthu kalikonse. Ameneyu ndi m’bale
wathu thupi limodzi ndi ife.” Abale ake anavomereza zimenezi.

28 Amalonda ena a ku Midiyani ankadutsa pomwepo. Tsono abale ake
a Yosefe anamutulutsa Yosefe uja mu chitsime chija ndipo anamugulitsa
kwa Aismaeli aja pamtengo wa masekeli makumi awiri. Choncho anapita
naye Yosefe ku Igupto.

29 Rubeni atabwerera ku chitsime kuja anapeza kuti Yosefe mulibe
m’chitsimemo. Pamenepo iye anang’amba zovala zake 30 nabwerera kwa

abale ake nati, “Mnyamata uja mulibemo! Nanga ndilowere kuti ine tsopano?”

31 Tsono anapha kamwana ka mbuzi, natenga mkanjo wa Yosefe ndi
kuwunyika m’magazi ake. 32 Iwo anatenga mkanjo uja nabwerera nawo
kwa abambo awo nati, “Ife tapeza mkanjowu. Tawuyang’anitsitsani muone ngati uli wa mwana wanu.”

33 Iye anawuzindikira ndipo anati, “Ndi mkanjo wa mwana wanga umenewu! Nyama yakuthengo yolusa yamudya. Mosakayika, mwana wanga Yosefe wakhadzulidwa.”

34 Pamenepo Yakobo anang’amba zovala zake, navala chisaka
m’chiwuno mwake. Iye analira maliro a mwana wake masiku ambiri.
35 Ngakhale kuti ana ake onse aamuna ndi aakazi anasonkhana kudzamutonthoza, iye anakana kutonthozedwa. Iye anati, “Ayi. Ndidzalira mpaka ndidzapite kwa mwana wanga ku manda.” Choncho Israeli anapitirirabe kulira mwana wake.

36 Amidiyani aja anagulitsa Yosefe kwa Potifara, mmodzi mwa nduna za Farao ku Igupto. Potifarayu anali mkulu wa asilikali olonda nyumba ya Farao.

# 38

### *Yuda ndi Tamara*

1 Pa nthawi imeneyi, Yuda anasiyana ndi abale ake napita kukakhala ndi
munthu wina wa ku Adulamu wotchedwa Hira. 2 Kumeneko, Yuda anaona
mwana wamkazi wa munthu wina wa Chikanaani wotchedwa Suwa.
Anamukwatira nagona naye malo amodzi. 3 Iye anatenga pathupi, nabala
mwana wamwamuna amene anamutcha Eri. 4 Anatenganso pathupi
nabala mwana wa mwamuna ndipo anamutcha Onani. 5 Anaberekanso
mwana wina wamwamuna ndipo anamutcha Sela. Ameneyu anabadwa Yuda ali ku Kezibi.

6 Yuda anamupezera mkazi mwana wake woyamba uja Eri, ndipo
dzina la mkaziyo linali Tamara. 7 Koma ntchito zoyipa za Eri, mwana
wachisamba wa Yuda zinayipira Yehova. Choncho Mulungu anamulanga ndi imfa.

8 Pamenepo Yuda anati kwa Onani, “Kwatira mkazi wamasiye wa m’bale
wako. Ulowe chokolo kuti m’bale wako akhale ndi mwana.” 9 Koma Onani
anadziwa kuti mwanayo sadzakhala wake. Choncho nthawi zonse pamene amagona naye mkaziyo, ankatayira umuna pansi kuti asamuberekere
mwana m’bale wake. 10 Zimene ankachitazi zinayipira Yehova. Choncho anamulanganso ndi imfa.

11 Kenaka Yuda anati kwa mpongozi wake Tamara, “Bwererani ku nyumba ya abambo anu ndi kukhala kumeneko ngati wamasiye mpaka mwana wanga Sela atakula.” Ananena izi chifukwa ankaopa kuti Sela angafenso ngati abale ake aja. Choncho Tamara anapita kukakhala ku nyumba ya abambo ake.

12 Patapita nthawi yayitali, Batishua, mkazi wa Yuda anamwalira. Yuda atatha kulira maliro a mkazi wake, anapita, iyeyu pamodzi ndi bwenzi lake Hira, Mwadulamu uja, ku Timna kumene ankameta nkhosa zawo.

13 Tamara atamva kuti apongozi ake akupita ku Timna kukameta
nkhosa, 14 iye anavula zovala zake za umasiye, nadziphimba nkhope ndi
nsalu kuti asadziwike, ndipo anakhala pansi pa chipata cha ku Enaimu

popita ku Timna. Tamara anachita izi chifukwa anaona kuti ngakhale
Selayo anali atakula tsopano, iye sanaperekedwe kuti amulowe chokolo.

15 Yuda atamuona anangomuyesa mkazi wadama chabe, chifukwa
anadziphimba nkhope. 16 Tsono anapita kwa mkaziyo pamphepete pa
msewu paja nati, “Tabwera ndigone nawe.” Apa Yuda sankadziwa kuti
mkazi uja anali mpongozi wake.

Ndiye mkazi uja anamufunsa Yuda nati, “Mudzandipatsa chiyani kuti
ndigone nanu?”

17 Iye anati, “Ndidzakutumizira kamwana kambuzi ka m’khola
mwanga.”

Mkaziyo anayankha kuti, “Chabwino, ndavomera, koma mungandipatse
chikole mpaka mutanditumizira mbuziyo?”

18 Iye anati, “Ndikupatse chikole chanji?”

Mkaziyo anayankha, “Mundipatse mphete yanuyo, chingwe chanucho
pamodzi ndi ndodo imene ili m’dzanja lanulo.” Choncho anazipereka kwa
iye nagona naye ndipo anatenga pathupi. 19 Kenaka Tamara anachoka,
navula nsalu anadziphimba nayo ija, navalanso zovala zake za umasiye
zija.

20 Tsono Yuda anatuma bwenzi lake Mwadulamu uja ndi kamwana kam-
buzi kaja kuti akapereke kwa mkazi wadama uja, ndi kuti akatero amub-
wezere chikole chake chija. Koma atafika sanamupezepo. 21 Anawafunsa
anthu a komweko, “Kodi mkazi wadama uja amene ankakhala pambali pa
msewu wa ku Enaimu, ali kuti?”

Iwo anayankha, “Sipanakhalepo mkazi wa dama aliyense pano.”

22 Choncho anabwerera kwa Yuda nati, “Sindinamupeze mkazi uja.
Kuwonjeza apo, anthu a kumeneko amati, ‘Sipanakhalepo mkazi wadama
pano.’ ”

23 Pamenepo Yuda anati, “Mulekeni atenge zinthuzo zikhale zake, kuopa
kuti anthu angatiseke. Ine sindinalakwe, ndinamutumizira kamwana
kambuzika, koma simunamupeze.”

24 Patapita miyezi itatu, Yuda anawuzidwa kuti, “Mpongozi wanu
Tamara anachita zadama, ndipo zotsatira zake n’zakuti ali ndi pathupi.”

Yuda anati, “Kamutulutseni ndipo mukamutenthe kuti afe!”

25 Akumutulutsa, iye anatuma mawu kwa apongozi ake. Anati,
“Ndili ndi pathupi pa munthu amene ndi mwini wake wa zinthu
izi. Taziyang’anitsitsani, kodi mwini wa khoza, chingwe ndi ndodo
yoyenderayi ndi yani?”

26 Yuda anazizindikira zinthuzo ndipo anati, “Uyu ndi wolungama
kuposa ine, chifukwa sindinamupereke kwa mwana wanga Sela.” Ndipo
Yuda sanagone nayenso.

27 Pamene Tamara nthawi inamukwanira yoti abeleke, m’mimbamo
munali mapasa. 28 Pamene ankabereka, mmodzi wa iwo anatulutsa dzanja
lake. Choncho mzamba anatenga kawulusi kofiira nakamangirira pa
mkono pa mwanayo nati, “Uyu ndiye anayamba kubadwa.” 29 Koma
pamene anabweza mkonowo, m’bale wake anabadwa ndipo mzamba
anati, “Wachita kudziphotcholera wekha njira chonchi!” Ndipo ana-
mutcha Perezi. 30 Pambuyo pake m’bale wake amene anali ndi ulusi
wofiira pa mkono wake uja anabadwa ndipo anapatsidwa dzina lakuti
Zera.

# 39

*Yosefe ndi Mkazi wa Potifara*

1 Tsopano Yosefe anatengedwa kupita ku Igupto. Potifara Mwigupto
amene anali mmodzi wa akuluakulu a Farao ndiponso mkulu wa asilikali
olonda ku nyumba kwa Farao, anagula Yosefe kwa Aismaeli amene anapita
naye kumeneko.
2 Koma Yehova anali ndi Yosefe ndipo zake zonse zimayenda bwino.
Iye ankakhala m'nyumba ya mbuye wake wa ku Igupto. 3 Mbuye wake
anaona kuti Yehova anali naye Yosefe ndi kuti pa chilichonse chimene
anachita Yehova ankaonetsetsa kuti achite bwino. 4 Potifara anakondwera
ndi Yosefe chifukwa cha matumikiridwe ake. Choncho anamusandutsa
woyang'anira nyumba yake ndi zonse za m'nyumba yake. 5 Kuchokera pa
nthawi imene anamuyika kukhala woyang'anira wa nyumbayo ndi zonse
za m'nyumbamo, Yehova anadalitsa nyumba ya Mwiguptoyo chifukwa cha
Yosefe. Madalitso a Yehova anali pa chilichonse chimene Potifara anali
nacho, za m'nyumba komanso za ku munda. 6 Choncho anasiyira m'manja
mwa Yosefe chilichonse chomwe anali nacho, kotero kuti samadandaula
ndi chilichonse kupatula chakudya chimene ankadya.
Tsopano Yosefe anali wa thupi labwino ndi wokongola. 7 Patapita
kanthawi, mkazi wa mbuye wake anayamba kusirira Yosefe nati, "Bwanji
ugone nane!"
8 Koma iye anakana namuwuza kuti, "Inu mukuona kuti mbuye wanga
sadandaula ndi kena kalikonse m'nyumba muno, ndipo chawo chilichonse
anachiyika m'manja mwanga. 9 Motero kuti palibe wina wamkulu kuposa
ine m'nyumba muno. Ndipo palibe chilichonse chimene mbuye wanga
sanachipereke kwa ine kupatula inuyo, chifukwa ndinu mkazi wake.
Tsono ndingachite bwanji choyipa choterechi ndi kuchimwira Mulungu?"
10 Ndipo ngakhale kuti iye anayankhula mawu omwewa ndi Yosefe tsiku
ndi tsiku, Yosefe sanalole kugona naye ngakhale kukhala naye pafupi.
11 Tsiku lina Yosefe analowa m'nyumbamo kukagwira ntchito zake,
ndipo munalibe wina aliyense wantchito m'nyumbamo. 12 Mkazi uja
anamugwira mkanjo Yosefe nati, "Tiye ugone nane!" Koma Yosefe anasiya
mkanjo wake m'manja mwa mkaziyo nathawira kunja kwa nyumba.
13 Pamene mkazi uja anaona kuti Yosefe wamusiyira mkanjo wake
m'manja mwake nathawira kunja kwa nyumba, 14 iye anayitana antchito
ake a m'nyumba nati, "Taonani mwamuna wanga anabwera ndi Mhebri
uyu m'nyumba muno kuti adzagone nane. Iyeyu analowa ku chipinda
kwanga kuti adzagone nane ndipo ine ndinakuwa kwambiri. 15 Atandimva
ndikukuwa, anandisiyira mkanjo wakewu n'kuthawira kunja."
16 Tsono mkazi wa Potifara uja anasunga mkanjowo mpaka mbuye
wake wa Yosefe atabwera ku nyumba. 17 Tsono anamuwuza nkhaniyi
nati: "Wantchito Wachihebri amene munatibweretsera uja anabwera kuti
adzagone nane. 18 Koma pamene ndinakuwa, iye anandisiyira mkanjo
wake nathawira kunja."
19 Mbuye wake wa Yosefe atamva nkhani imene mkazi wake ana-
muwuza kuti, "Ndi zimene anandichitira wantchito wanu," anapsa mtima
kwambiri. 20 Tsono iye anatenga Yosefe namuyika m'ndende mmene
ankasungiramo am'ndende a mfumu.
Ndipo Yosefe anakhala m'ndendemo 21 koma Yehova anali naye,
ndipo anamuonetsa kukoma mtima kwake, kotero kuti woyang'anira

ndende anakondwera ndi Yosefe. 22 Choncho woyang'anira ndende
uja anamuyika Yosefe kukhala woyang'anira onse amene anayikidwa
m'ndende. Ndiponso anamupatsa udindo woyang'anira zonse zochitika
m'ndendemo. 23 Woyang'anira ndende uja sankayang'aniranso china
chilichonse chimene chinali mu ulamuliro wa Yosefe, chifukwa Yehova
anali ndi Yosefe. Ndipo Yehova anaonetsetsa kuti chilichonse chimene
Yosefe ankachita chimuyendere bwino.

# 40

*Yosefe Amasulira Maloto a Am'ndende Anzake*

1 Patapita nthawi, woperekera zakumwa ndi wopanga buledi a
ku nyumba kwa mfumu ya ku Igupto analakwira mbuye wawoyo.
2 Farao anapsa mtima ndi akuluakulu awiriwa, 3 ndipo anakawatsekera
m'ndende, nakawayika m'manja mwa mkulu wa asilikali olonda ku
nyumba kwa mfumu kuja, m'ndende momwe Yosefe ankasungidwamo.
4 Mkulu wa alonda aja anawapereka m'manja mwa Yosefe, ndipo iye
anawasamalira.

Iwo anakhala m'ndendemo kwa kanthawi. 5 Usiku wina, aliyense wa
anthu awiriwa, wopereka zakumwa pamodzi ndi wopanga buledi wa ku
nyumba ya mfumu ya ku Igupto aja, amene ankasungidwa m'ndende,
analota maloto. Malotowo anali ndi tanthauzo lake.

6 Mmawa wake, Yosefe atabwera, anaona kuti nkhope zawo zinali
zakugwa. 7 Choncho anafunsa akuluakulu a kwa Farao amene anali naye
m'ndende muja kuti, "Bwanji nkhope zanu zili zachisoni lero?"

8 Iwo anayankha, "Tonse awiri talota maloto, koma palibe wotitan-
thauzira malotowo."

Pamenepo Yosefe anawawuza kuti, "Ndi Mulungu yekha amene
amapereka matanthauzo a maloto. Uzeni ine maloto anu."

9 Choncho mkulu wa operekera zakumwa uja anamuwuza Yosefe maloto
ake. Anati, "M'maloto anga ndinaona mtengo wa mpesa, 10 unali
ndi nthambi zitatu. Mpesawo utangophukira, unachita maluwa ndipo
maphava ake anabereka mphesa zakupsa. 11 Chikho cha Farao chinali
m'manja mwanga, ndipo ndinatenga mphesa, kupsinyira mu chikho cha
Farao ndi kuchipereka m'manja mwake."

12 Yosefe anati kwa iye, "Tanthauzo lake ndi ili: Nthambi zitatuzo ndi
masiku atatu. 13 Pakangopita masiku atatu, Farao adzakutulutsa muno.
Udzaperekera zakumwa kwa Farao monga momwe umachitira poyamba.
14 Koma zako zikakuyendera bwino, udzandikumbukire ndi kundikomera
mtima. Chonde ukandipepesere kwa Farao kuti anditulutse muno.
15 Popezatu ine anangochita mondiba kubwera nane kuno kuchokera ku
dziko la Ahebri, ndipo ngakhale kunoko, ine sindinalakwe kali konse kuti
ndizipezeka m'dzenje muno."

16 Mkulu wa opanga buledi ataona kuti Yosefe wapereka tanthauzo
labwino, anati kwa Yosefe, "Inenso ndinalota nditasenza nsengwa zitatu za
buledi. 17 Mu nsengwa yapamwamba munali zakudya zamitundumitundu
za Farao, koma mbalame zimadya zakudyazo."

18 Yosefe anati, "Tanthauzo lake ndi ili: nsengwa zitatuzo ndi masiku
atatu. 19 Pakangotha masiku atatu Farao adzakutulutsa muno koma
adzakupachika. Ndipo mbalame zidzadya mnofu wako."

[20] Tsono tsiku lachitatulo linali lokumbukira kubadwa kwa Farao, ndipo anawakonzera phwando akuluakulu ake onse. Anatulutsa m'ndende mkulu wa operekera zakumwa ndi mkulu wa ophika buledi, ndipo
anawayimiritsa pamaso pa nduna zake. [21] Tsono Farao anamubwezera mkulu wa operekera zakumwa uja pa udindo wake, kotero kuti anayamba
kuperekeranso zakumwa kwa Farao, [22] koma mkulu wa ophika buledi
anamupachika, mofanana ndi mmene Yosefe anatanthauzira maloto.
[23] Koma mkulu wa operekera zakumwa uja sanamukumbukire Yosefe ndipo anamuyiwaliratu.

# 41

*Maloto a Farao*

[1] Patapita zaka ziwiri zathunthu, Farao analota atayimirira m'mbali
mwa mtsinje wa Nailo, [2] ndipo anangoona ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri zooneka bwino ndi zonenepa zikutuluka mu mtsinje muja
ndi kuyamba kudya msipu wa mu mawango. [3] Kenaka ng'ombe zina zazikazi zisanu ndi ziwiri zosaoneka bwino ndi zowonda zinatulukanso mu mtsinje wa Nailo ndipo zinayimirira pambali pa zina zija zimene
zinali m'mphepete mwa mtsinje uja. [4] Ndipo ng'ombe zosaoneka bwino ndi zowonda zija zinadya ng'ombe zonenepa zija. Kenaka Farao anadzidzimuka.
[5] Posakhalitsa anagonanso ndipo analota kachiwiri: Analota ngala zisanu ndi ziwiri za tirigu zathanzi labwino zitabala pa phata limodzi.
[6] Kenaka ngala zina zisanu ndi ziwiri zinaphuka. Izi zinali zowonda ndi
zowauka ndi mphepo ya kummawa. [7] Ngala zowonda zija zinameza ngala zathanzi ndi zonenepa zija. Farao anadzidzimuka ndipo anaona kuti anali maloto chabe.
[8] Mmawa, Farao anavutika mu mtima kotero anayitanitsa amatsenga ndi anzeru onse a mu Igupto. Iwo atabwera, iye anawawuza maloto ake, koma panalibe ndi mmodzi yemwe amene anatha kutanthauzira malotowo kwa Farao.
[9] Ndipo mkulu wa operekera zakumwa anati kwa Farao, "Lero ndakum-
bukira kulephera kwanga. [10] Paja nthawi ina Farao anapsera mtima antchito akefe, ndipo anatitsekera (ine ndi mkulu wa ophika buledi)
m'ndende, m'nyumba ya mkulu wa alonda. [11] Tsiku lina tonse awiri
tinalota maloto, ndipo loto lililonse linali ndi tanthauzo lake. [12] Tsono momwemo munali mnyamata wina Wachihebri, wantchito wa mkulu wa alonda. Ife tinamufotokozera maloto athu, ndipo anatitanthauzira
malotowo. Munthu aliyense anamupatsa tanthauzo la loto lake. [13] Ndipo zinthu zinachitikadi monga mmene anatitanthauzira. Ine anandibwezera pa ntchito yanga ndipo winayo anapachikidwa."
[14] Choncho Farao anamuyitanitsa Yosefe, ndipo mofulumira anabwera naye kuchokera m'dzenje muja. Ndipo atameta, ndi kusintha zovala, anapita kwa Farao.
[15] Farao anati kwa Yosefe, "Ndinalota maloto ndipo palibe amene watha kunditanthauzira. Tsono ndawuzidwa kuti iwe ukamva loto umadziwanso kulimasulira."
[16] Yosefe anamuyankha Farao kuti, "Sindingathe koma Mulungu apereka yankho limene Farao akufuna."
[17] Ndipo Farao anati kwa Yosefe, "Ndinalota nditayimirira m'mphepete
mwa mtsinje wa Nailo, [18] ndipo ng'ombe zisanu ndi ziwiri zonenepa ndi

zooneka bwino zinatuluka mu mtsinje muja ndi kumadya msipu wa mu
mawango. 19 Kenaka, ng'ombe zina zisanu ndi ziwiri zinatuluka. Izi
zinali zosaoneka bwino ndiponso zowonda ndipo sindinaonepo ng'ombe
zosaoneka bwino chonchi m'dziko lonse la Igupto. 20 Ng'ombe zosaoneka
bwino ndi zowonda zija zinadya zisanu ndi ziwiri zonenepa zimene zinat-
uluka poyamba zija. 21 Koma ngakhale ng'ombezi zinadya zinazo, palibe
amene akanatha kuzindikira kuti zinatero popeza zinali zosaonekabe
bwino monga poyamba. Ndipo ndinadzidzimuka.

22 "Nditagonanso kachiwiri, ndinalota ngala zisanu ndi ziwiri za tirigu
zathanzi ndi zonenepa zitabala pa phata limodzi. 23 Kenaka panaphukanso
ngala zina zisanu ndi ziwiri zofota, zowonda ndi zowauka ndi mphepo ya
kummawa. 24 Ngala zowondazo zinameza ngala zisanu ndi ziwiri zabwino
zija. Ndinawawuza amatsenga koma palibe ndi mmodzi yemwe anatha
kundimasulira."

25 Ndipo Yosefe anati kwa Farao, "Maloto awiriwa ndi ofanana ndipo
ali ndi tanthauzo limodzi. Mulungu waululira Farao chimene atachite.
26 Ng'ombe zisanu ndi ziwiri zabwinozo ndi zaka zisanu ndi ziwiri. Ndipo
ngala zisanu ndi ziwiri zabwinozo ndi zaka zisanu ndi ziwiri. Kutanthauza
kwa maloto n'kumodzi. 27 Ng'ombe zisanu ndi ziwiri zowonda ndi
zosaoneka bwino zimene zinatuluka pambuyozo ndiponso ngala zisanu
ndi ziwiri zachabechabe, zowauka ndi mphepo ya kummawa zija ndi zaka
zisanu ndi ziwiri za njala.

28 "Tsono ndi monga ndafotokozeramu kuti Mulungu wakuwuziranitu
zimene adzachite. 29 Zaka zisanu ndi ziwiri za zokolola zochuluka
zikubwera mu dziko lonse la Igupto, 30 koma zidzatsatana ndi zaka zina
zisanu ndi ziwiri za njala. Chakudya chochuluka cha mu Igupto chija
chidzayiwalika ndipo njalayo idzawononga dziko. 31 Zakudya zochuluka
za m'dzikomo zija sizidzakumbukirikanso chifukwa njala imene iti idzab-
wereyo idzakhala yoopsa. 32 Popeza kuti malotowa aperekedwa kwa inu
Mfumu kawiri, ndiye kuti Mulungu watsimikiza kuti adzachitadi zimenezi
posachedwapa.

33 "Tsopano Farao apezeretu munthu wozindikira ndi wanzeru ndipo
amuyike kukhala woyang'anira dziko lonse la Igupto. 34 Asankhenso
akuluakulu a m'dziko lino. Iwowa azitenga ndi kuyika padera limodzi
la magawo asanu aliwonse a zokolola za m'dziko muno mu zaka zonse
zisanu ndi ziwiri za chakudya chochuluka. 35 Iwo asonkhanitse zakudya
zonse za m'zaka zabwino zikubwerazi. Pansi pa ulamuliro wa Farao,
akuluakuluwo asonkhanitse ndi kusunga bwino tirigu m'mizinda yonse.
36 Chakudya chimenechi chisungidwe kuti chidzagwiritsidwe ntchito
m'zaka zisanu ndi ziwiri za njala imene ikubwerayo mu Igupto, kuti anthu
a m'dzikoli asadzafe ndi njalayo."

37 Farao ndi nduna zake anagwirizana nawo malangizo a Yosefe.
38 Choncho Farao anafunsa nduna zake nati, "Kodi tingathe kumupeza
munthu wina ngati uyu, amene ali ndi mzimu wa Mulungu?"

39 Farao anati kwa Yosefe, "Pakuti Mulungu wakudziwitsa iwe zonsezi,
palibe wina wodziwa zinthu ndi wanzeru ngati iwe. 40 Iwe ukhala nduna
yayikulu mu dziko langa ndipo anthu onse adzamvera zimene walamula.
Ine ndekha ndiye amene ndidzakuposa mphamvu chifukwa ndimakhala
pa mpando waufumu."

### *Yosefe Alamulira Dziko la Igupto*

[41] Choncho Farao anati kwa Yosefe, “Ine ndikukuyika iwe kukhala nduna
yoyang’anira dziko lonse la Igupto.” [42] Ndipo Farao anavula mphete
ku chala chake nayiveka ku chala cha Yosefe. Anamuvekanso mkanjo
wonyezimira ndi nkufu wagolide m’khosi mwake. [43] Anamukweza Yosefe
pa galeta ngati wachiwiri pa ulamuliro. Ndipo anthu anafuwula pamaso
pake nati, “M’gwadireni!” Motero anakhala nduna yayikulu ya dziko lonse
la Igupto.

[44] Kenaka Farao anati kwa Yosefe, “Ine ndine Farao; tsono iwe ukapanda
kulamula, palibe amene akhoza kuchita chilichonse ngakhale kuyenda
kumene m’dziko lonse la Igupto.” [45] Farao anamupatsa Yosefe dzina
lakuti Zafenati-Panea ndipo anamupatsanso Asenati mwana wa mkazi wa
Potifara, wansembe wa Oni, kuti akhale mkazi wake. Choncho Yosefe
anayendera dziko lonse la Igupto.

[46] Yosefe anali ndi zaka 30 pamene amayamba ntchito kwa Farao,
mfumu ya ku Igupto. Ndipo Yosefe anachoka pa maso pa Farao
nayendera dziko lonse la Igupto. [47] M’zaka zisanu ndi ziwiri za
zokolola zambiri zija, anthu m’dzikomo anakolola zochuluka. [48] Yosefe
anasonkhanitsa zakudya zonse zokololedwa m’zaka zisanu ndi ziwiri zija
ndipo anazisunga m’mizinda. Mu mzinda uliwonse anayikamo chakudya
chimene chinalimidwa m’minda yozungulira komweko. [49] Yosefe ana-
sunga tirigu wochuluka kwambiri ngati mchenga wa ku nyanja. Kunali
tirigu wochuluka kwambiri motero kuti analeka n’kulembera komwe.

[50] Zisanafike zaka zanjala, Yosefe anabereka ana aamuna awiri mwa
Asenati mwana wa mkazi wa Potifara, wansembe wa Oni. [51] Yosefe
anamutcha mwana wake woyamba, Manase popeza anati, “Mulungu
wandiyiwalitsa zovuta zanga zija ndiponso banja la abambo anga.”
[52] Mwana wachiwiri wa mwamuna anamutcha Efereimu popeza anati,
“Mulungu wandipatsa ana m’dziko la masautso anga.”

[53] Zaka zisanu ndi ziwiri za zokolola zochuluka zija zinatha, [54] ndipo
zaka zisanu ndi ziwiri za njala zija zinayamba monga ananenera Yosefe.
Njalayi inafika ku mayiko ena onse koma ku dziko lonse la Igupto kunali
chakudya. [55] Pamene njala ija inakwanira dziko lonse la Igupto anthu
analilira Farao kuti awapatse chakudya. Koma Farao anawawuza kuti,
“Pitani kwa Yosefe ndipo mukachite zimene akakuwuzeni.”

[56] Pamene njala inafalikira dziko lonse, Yosefe anatsekula nkhokwe
za zakudya namagulitsa tirigu kwa anthu a ku Igupto aja, pakuti njala
inafika poyipa kwambiri mu Igupto monse. [57] Anthu ankabwera ku Igupto
kuchokera ku mayiko ena onse kudzagula tirigu kwa Yosefe, chifukwa
njala inafika poyipa kwambiri pa dziko lonse lapansi.

# 42

*Abale a Yosefe Apita ku Igupto*

[1] Yakobo atamva kuti ku Igupto kuli tirigu, anati kwa ana ake,
“N’chifukwa chiyani mukungoyang’anana wina ndi mnzake? [2] Ine
ndamva kuti ku Igupto kuli tirigu. Pitani kumeneko mukatigulireko kuti
tisafe ndi njala.”

[3] Choncho abale ake khumi a Yosefe anapita kukagula tirigu ku Igupto.
[4] Koma Yakobo sanamulole Benjamini mng’ono wake wa Yosefe kuti apite
nawo chifukwa anaopa kuti choyipa chingamuchitikire. [5] Choncho ana a

Israeli aja anapita pamodzi ndi gulu la anzawo kukagula tirigu pakuti ku Kanaani kunalinso njala.

6 Pakuti Yosefe anali nduna yayikulu yolamulira dziko la Igupto, ndiye kuti analinso amene ankagulitsa tirigu kwa anthu onse. Choncho abale
ake a Yosefe nawonso anabwera, ndipo anamugwadira pansi. 7 Yosefe
atangowaona abale ake anawazindikira, koma ananamizira kukhala ngati mlendo nawayankhula mwaukali kuwafunsa kuti, "Mwachokera kuti?"

Iwo anayankha, "Ku dziko la Kanaani, tikudzagula chakudya."

8 Ngakhale Yosefe anawazindikira abale ake, koma iwo sanamuzindikire.
9 Pamenepo anakumbukira maloto aja amene analota za iwo ndipo anati, "Inu ndinu akazitape! Mwabwera kudzazonda dziko lathu kuti muone pamene palibe chitetezo."

10 Iwo anayankha, "Ayi mbuye wathu, antchito anufe tabwera kudzagula
chakudya. 11 Tonse ndife ana a munthu mmodzi. Ndife antchito anu okhulupirika osati akazitape."

12 Iye anawawuza kuti, "Ayi! Inu mwabwera kudzaona pamene palibe chitetezo m'dziko muno."

13 Koma iwo anayankha, "Tinalipo ana aamuna khumi ndi awiri. Abambo athu ndi mmodzi, ndipo kwathu ndi ku Kanaani. Panopo wotsiriza ali ndi abambo athu ndipo wina anamwalira."

14 Yosefe anawawuza kuti, "Ndi momwe ndaneneramo: Inu ndinu
akazitape. 15 Ndiye ndikuyesani motere: Ine ndikulumbira pali Farao nndithu, inuyo simudzachoka malo ano mpaka wotsirizayo atabwera kuno.
16 Tumizani mmodzi wa inu akamutenge m'bale wanuyo ndipo ena nonsenu musungidwa m'ndende, kuti titsimikize ngati zimene mukunenazi
ndi zoona. Apo ayi, pali Farao ndithu, inu ndinu akazitape!" 17 Ndipo
onse anawayika m'ndende kwa masiku atatu.

18 Pa tsiku lachitatu Yosefe anawawuza kuti, "Popeza ine ndimaopa Mulungu, ndipo inuyo ngati mukufuna kukhala ndi moyo muchite izi:
19 Ngati muli anthu achilungamo, mmodzi wa inu atsale m'ndende, pamene ena nonse mupite kwanu kuti muwatengere chakudya anthu
akwanu kuli njalako. 20 Mukabwere naye kuno mng'ono wanu wotsirizayo
kuti titsimikizire zimene munanena kuti musafe." Ndipo anachita zomwezo.

21 Iwo anati kwa wina ndi mnzake, "Ndithu ife tinalakwira m'bale wathu uja popeza kuti ngakhale tinaona kuvutika kwake ndi kumva kulira kwake pamene ankatidandaulira kuti timuchitire chifundo, koma ife sitinamvere. N'chifukwa chake masautso awa atigwera."

22 Rubeni anayankha, "Kodi sindinakuwuzeni kuti musamuchite kanthu mnyamata uja? Koma inu simunamvere! Tsopano tikulandira malipiro
a magazi ake." 23 Koma sanadziwe kuti Yosefe ankawamva popeza kuti ankagwiritsa ntchito wotanthauzira poyankhula naye.

24 Yosefe anapita pambali payekha kukalira. Kenaka anabweranso nadzayankhula nawo. Iye anatenga Simeoni namumanga iwo akuona.

25 Yosefe analamula kuti awadzazire matumba awo ndi tirigu, awayikiremo ndalama zawo momwemo ndiponso awapatse chakudya cha
panjira. Izi anawachitiradi. 26 Abale a Yosefe aja anasenzetsa abulu awo
tirigu amene anagula uja ndipo ananyamuka ulendo wawo.

27 Atafika pamalo pena poti agone, mmodzi mwa iwo anatsekula thumba lake kuti atapemo chakudya cha bulu wake. Atangomasula anaona kuti

ndalama zake zili pakamwa pa thumba. 28 Iye anati kwa abale akewo,
“Ndalama zanga andibwezera, izi zili m’thumba mwangamu.”
Mitima yawo inachita ngati yachokamo ndipo anali ndi mantha ambiri, nati, “Ndi chiyani chimene Mulungu watichitira?”
29 Atafika kwa abambo awo Yakobo m’dziko la Kanaani anafotokoza
zonse zimene zinawachitikira nati, 30 “Nduna yayikulu ya m’dzikomo
inatiyankhula mwa ukali kwambiri ndipo inkatiyesa kuti ndife akazitape.
31 Koma tinamuwuza kuti, ‘Ndife anthu woona mtima osati
akazitape. 32 Ife tonse tinalipo ana aamuna khumi ndi awiri, abambo mmodzi. Mmodzi anamwalira, ndipo wamng’ono ali ndi abambo athu ku Kanaani.’ ”
33 Ndipo nduna ija inati kwa ife, “Kuti ndidziwedi kuti ndinu anthu owona mtima muchite izi: Mmodzi mwa inu atsale ndi ine kuno, ndipo enanu mutenge chakudya ndi kubwerera kwanu kumene kuli njalako.
34 Koma mundibweretsere wotsirizayo kuti ndidziwedi kuti
sindinu akazitape koma anthu achilungamo. Kenaka ndidzakubwezerani m’bale wanuyu ndipo mukhoza kuchita malonda m’dzikoli.”
35 Pamene amakhuthula matumba awo a tirigu aliyense anapeza kuti kathumba kake ka ndalama kali momwemo. Ataona zimenezi, iwo
pamodzi ndi abambo awo anachita mantha kwambiri. 36 Abambo awo
Yakobo anawawuza kuti, “Mwandilanda ana anga ine. Yosefe anamwalira ndipo Simeoni palibenso, ndiye tsopano mukufuna mutengenso Benjamini. Zonsezi zandigwera ine!”
37 Koma Rubeni anati kwa abambo ake, “Ngati sindidzabwera naye kwa inu, mudzaphe ana anga aamuna awiri. Mupereken m’manja mwangamu ndipo ndidzamusamala ndi kubwera naye kwa inu.”
38 Koma Yakobo anati, “Mwana wanga sapita nanu kumeneko; mkulu wake anamwalira ndipo watsala yekha. Ngati choyipa chitamuchitikira pa ulendo mukupitawu, ndiye kuti ndi mmene ndakalambiramu inu mudzandipha ndi chisoni chotere.”

# 43

*Ulendo Wachiwiri wa ku Igupto*
1 Njala inakula kwambiri m’dzikomo. 2 Tsono atatha kudya tirigu yense
amene anakatenga ku Igupto, Yakobo anati kwa ana ake aja, “Pitani kuti mukatigulire chakudya china pang’ono.”
3 Koma Yuda anati kwa iye, “Munthu uja anatichenjeza monenetsa kuti, ‘Simudzandionanso ine pokhapokha mutabwera ndi mng’ono
wanu.’ 4 Mukalola kuti mng’ono wathuyu apite nafe, ndiye ife tidzapita
kukakugulirani chakudya. 5 Koma mukapanda kumulola, ife sitipita, chifukwa munthuyo anatiwuza kuti, ‘Simudzandionanso pokhapokha mutabwera ndi mng’ono wanuyo.’ ”
6 Tsono Israeli anafunsa kuti, “Bwanji inu munandiputira mavuto oterewa pomuwuza munthuyo kuti muli ndi m’bale wanu wina?”
7 Iwo anayankha, “Munthuyo ankangofunsafunsa za ife ndi za banja lathu. Iye anatifunsa kuti, ‘Kodi abambo anu akanali ndi moyo? Kodi muli ndi m’bale wanu wina?’ Ife tinkangoyankha mafunso ake. Ife tikanadziwa bwanji kuti adzanena kuti, ‘Mubwere naye kuno m’bale wanu’?”
8 Ndipo Yuda anati kwa Israeli abambo ake, “Mululeni mnyamatayo apite ndi ine, ndipo tinyamuka nthawi yomweyo, kuti ife ndi inu pamodzi
ndi ana athu tikhale ndi moyo. 9 Ine ndidzipereka kuti ndikhale chikole

cha moyo wa mnyamatayu. Ine ndidzamuteteza. Ngati sindibwera naye
ndi kumupereka kwa inu, ndidzakhala wolakwa pamaso panu moyo
wanga wonse. 10 Mmene zililimu, tikanapanda kuchedwa, bwenzi titapita
ndi kubwerako kawiri."
11 Tsono abambo awo Israeli anawawuza kuti, "Ngati pafunika kutero,
ndiye muchite izi: Ikanimo zipatso zabwino kwambiri za dziko lino
m'matumba mwanu ndi kumutengera munthuyo ngati mphatso. Mu-
mutengere mafuta wopaka pang'ono, uchi pang'ono, mafuta wonunkhir-
itsa chakudya, mule, mtedza ndi alimoni. 12 Mutenge ndalama zokwanira.
Ndalama zina n'zokamubwezera zija anakuyikirani m'matumba anu
zija. Mwina anangolakwitsa. 13 Mutengeninso mng'ono wanuyu ndi
kubwerera kwa munthuyo msanga. 14 Ndipo Mulungu Wamphamvuzonse
akuchitireni chifundo pamaso pa munthuyo kuti akamulole m'bale wanu
wina uja ndi Benjamini kuti abwerere ndi inu. Kukakhala kulira, ndine
wolira basi."
15 Choncho abale aja anatenga mphatso, ndalama zokwanira ndi
Benjamininso. Iwo anafulumira kupita ku Igupto ndipo anakaonekera
kwa Yosefe. 16 Yosefe ataona Benjamini ali pamodzi ndi abale ake,
anati kwa wantchito wa m'nyumba mwake, "Atengereni anthu awa ku
nyumba kwanga, ndipo uphe nyama ndi kukonza bwino chakudya popeza
amenewa adya ndi ine masana ano."
17 Wantchitoyo anachita monga momwe Yosefe ananenera, ndipo
anawatengera abale aja ku nyumba kwa Yosefe. 18 Tsono anthu aja
anachita mantha ataona kuti akuwatengera ku nyumba kwa Yosefe.
M'maganizo awo ankanena kuti, "Atibweretsa kuno chifukwa cha
ndalama zija zinabwezeredwa m'matumba athu poyamba paja. Ameneyu
akufuna kuti atipanikize ndi kutigwira ukapolo natilanda abulu athu."
19 Choncho atafika pa khomo la nyumba ya Yosefe anamuyandikira
wantchito wa Yosefe nayankhula naye kuti, 20 "Pepani mbuye wathu,
ife tinabweranso ulendo woyamba kudzagula chakudya 21 koma titafika
pa malo ena kuti tigone, tinatsekula matumba athu ndipo aliyense wa
ife anapeza ndalama zake momwe zinalili zili pakamwa pa thumba
lake. Ndiye tabwerera nazo. 22 Tabweretsanso ndalama zina kuti tigule
chakudya. Sitikudziwa kuti kaya ndani anayika ndalamazo m'matumba
athu."
23 Koma iye anati, "Mitima yanu ikhale pansi ndipo musachite mantha.
Mulungu wanu, Mulungu wa abambo anu, anakuyikirani chumacho
m'matumba anu. Ine ndinalandira ndalama zanu." Ndipo anakawatu-
lutsira Simeoni.
24 Wantchito uja anawalowetsa anthuwo m'nyumba ya Yosefe, nawap-
atsa madzi kuti asambe mapazi awo. Anadyetsanso abulu awo. 25 Abale
aja anakonzeratu mphatso zawo zija kuti adzapereke kwa Yosefe, popeza
anamva kuti Yosefe adzadya komweko masana.
26 Yosefe atafika ku nyumbako, iwo anapereka mphatso zija namuw-
eramira pansi. 27 Yosefe anawafunsa za moyo wawo kenaka anati, "Kodi
abambo anu wokalamba amene munkandiwuza aja ali bwanji? Ali ndi
moyobe?"
28 Iwo anayankha kuti, "Mtumiki wanu abambo athu akanali ndi moyo
ndipo ali bwino." Ndipo anamugwadira namuweramira pansi.
29 Pomwazamwaza maso Yosefe anaona Benjamini, m'bale wake weni-
weni wa bere limodzi, ndipo anafunsa, "Kodi uyu ndiye m'bale wanu

wamng’ono kwambiri amene munkandiwuza uja?” Kenaka anati, “Am-
buye akukomere mtima mwana wanga.” 30 Kenaka Yosefe anafulumira
kutuluka chifukwa mtima wake unadzaza ndi chifundo cha mng’ono wake
ndipo anafuna kulira. Tsono anakalowa m’chipinda chakechake nakalira
kumeneko.

31 Atatha kupukuta misozi m’maso mwake anatuluka, ndipo modzilim-
bitsa analamula kuti chakudya chibwere.

32 Anamupatsira Yosefe chakudya payekha, abale ake aja pawokha,
ndiponso Aigupto amene ankadya pamodzi ndi iye nawonso pawokha.
Izi zinali choncho chifukwa Aigupto ankanyansidwa kudya pamodzi ndi
Ahebri. 33 Abale aja anawakhazika patsogolo pa Yosefe. Iwo anawak-
hazika monga mwa mabadwidwe awo kuyambira woyamba kubadwa
mpaka wotsirizira; ndipo ankangoyang’anitsitsana modabwa. 34 Tsono
ankawagawira chakudya kuchokera pa tebulo la Yosefe. Koma chakudya
cha Benjamini chinkaposa cha ena onsewa kasanu. Motero anadya ndi
kumwa mpaka kukhuta, ndipo anasangalala pamodzi ndi Yosefe.

# 44

### *Chikho Chasiliva M’thumba la Benjamini*

1 Pambuyo pake Yosefe analamulira wantchito wa m’nyumba mwake
kuti, “Adzazire chakudya anthuwa m’matumba mwawo monga mmene
anganyamulire, ndipo uwayikire ndalama zawo pakamwa pa matumba
awowo. 2 Tsono uyike chikho changa cha siliva chija, pakamwa pa thumba
la wamng’ono kwambiriyu pamodzi ndi ndalama zake za chakudya”
Ndipo iye anachita monga Yosefe ananenera.

3 Mmawa kutacha anthu aja analoledwa kuti apite ndi abulu awo.
4 Atangotuluka mu mzinda muja, koma asanapite patali, Yosefe anati kwa
wantchito wake, “Nyamuka atsatire anthu aja msanga. Ndipo ukawapeza,
uwafunse kuti, ‘Bwanji mwabwezera zoyipa ndi zabwino? 5 Mwaberanji
chikho chimene mbuye wanga amamweramo ndi kugwiritsa ntchito
akafuna kuwombeza? Chimene mwachitachi ndi chinthu choyipa.’ ”

6 Wantchito uja atawapeza ananena mawu anawuzidwa aja. 7 Koma iwo
anati kwa iye, “Kodi mbuye wanga mukuneneranji zimenezi? Sizingath-
eke ndi pang’ono pomwe kuti antchito anufe n’kuchita zoterozo ayi! 8 Paja
ife pobwera kuchokera ku Kanaani tinatenga ndalama kubwezera zimene
tinazipeza m’matumba mwathu. Ndiye pali chifukwa chanji kuti tikabe
siliva kapena golide m’nyumba mwa mbuye wanu? 9 Ngati wantchito
wanu wina pano atapezeka nacho chikhocho, ameneyo aphedwe ndipo
ena tonsefe tidzakhala akapolo anu, mbuye wathu.”

10 Iye anati, “Chabwino, tsono zikhale monga mwaneneramu. Komatu
aliyense amene angapezeke nacho chikhocho adzakhala kapolo wanga,
ndipo ena nonsenu muzipita mwaufulu.”

11 Tsono onse anafulumira kutsitsa pansi aliyense thumba lake ndi
kulitsekula. 12 Kenaka anayamba kufufuza, kuyambira pa wamkulu
mpaka pa wamng’ono. Ndipo chikhocho chinapezeka m’thumba mwa
Benjamini. 13 Apo onse anang’amba zovala zawo ndi chisoni. Ndipo
anasenzetsa abulu katundu wawo nabwerera ku mzinda konkuja.

14 Pamene Yuda ndi abale ake ankafika ku nyumba kwa Yosefe n’kuti
Yosefe akanali komweko. Ndipo anadzigwetsa pansi pamaso pake.

15 Yosefe anafunsa kuti, “N’chiyani mwachitachi? Kodi simudziwa kuti
munthu ngati ine ndikhoza kuona zinthu mwakuwombeza?”

16 Yuda anayankha, “Kodi tinganenenji kwa mbuye wanga? Tinena
chiyani? Tingadzilungamitse bwanji? Mulungu waulula kulakwa kwa
antchito anu. Ndipo tsopano ndife akapolo a mbuye wanga, ife tonse
pamodzi ndi amene wapezeka ndi chikhocho.”

17 Koma Yosefe anati, “Sindingachite choncho ayi! Yekhayo amene
wapezeka ndi chikhocho ndi amene akhale kapolo wanga. Ena nonsenu,
bwererani kwa abambo anu mu mtendere.”

18 Ndipo Yuda anamuyandikira iye nati, “Chonde mbuye wanga mulole
kapolo wanune ndinene mawu pang’ono kwa mbuye wanga. Mu-
sandipsere mtima, kapolo wanune, popeza inu muli ngati Farao yemwe.
19 Mbuye wanga munafunsa akapolo anufe kuti, ‘Kodi muli ndi abambo
anu kapena m’bale wanu?’ 20 Ndipo ife tinayankha, ‘Inde mbuye wathu,
ife tili ndi abambo athu wokalamba, ndipo pali mwana wamwamuna
wamng’ono amene anabadwa abambo athu atakalamba kale. M’bale
wake anafa ndipo ndi yekhayo m’mimba mwa amayi ake amene watsala
ndipo abambo ake amamukonda.’

21 “Ndipo inu munatiwuza kuti, ‘Mubwere naye kwa ine kuti ndidza-
muone ndekha.’ 22 Ife tinati, ‘Mbuye wathu, mnyamatayo sangasiye
abambo ake, akawasiya ndiye kuti abambo akewo adzafa.’ 23 Koma
inu munatichenjeza kuti, ‘Pokhapokha mutabwera naye m’bale wanu
wamng’ono kwambiri, simudzandionanso.’ 24 Ndiye pamene tinafika kwa
kapolo wanu, abambo athu tinawawuza zonse zimene munanena.

25 “Abambo athu anatiwuza kuti, ‘Pitaninso mukagule kachakudya
pang’ono.’ 26 Koma tinati, ‘Sitingathe kupitanso. Sitingapite pokhapokha
mng’ono wathuyu apite nafe chifukwa munthu uja anati sitingaonane
naye ngati mng’ono wathuyu sakhala nafe.’

27 “Koma kapolo wanu, abambo athu anatiwuza kuti, ‘Inu mukudziwa
kuti mkazi wanga anandiberekera ana aamuna awiri. 28 Mmodzi wa iwo
anandisiya. Ine ndimati anadyedwa ndi chirombo popeza sindinamuo-
nenso mpaka lero. 29 Tsopano mukanditengeranso uyu, nakaphedwa mu
njira ndiye kuti mudzandikankhira ku manda ndi chisoni.’

30 “Tsono ngati tizibwerera kwa mtumiki wanu, abambo athu popanda
mnyamatayu, amene moyo wa abambo ake uli pa iyeyu, 31 ndipo
akakaona kuti mnyamatayu palibe, basi akafa. Ife tidzakhala ngati
takankhira abambo athu ku manda ndi chisoni. 32 Ndiponsotu ine
ndinadzipereka kwa abambo anga kukhala chikole chotsimikiza kuti
mnyamatayu ndidzamuteteza, ndipo ndinati, ‘Ngati sindibwerera naye
mnyamatayu kwa inu, ndiye kuti ndidzakhala wochimwira inu abambo
anga moyo wanga wonse.’

33 “Tsono, chonde mulole kuti ine kapolo wanu nditsalire kuno kukhala
kapolo wa mbuye wathu m’malo mwa mnyamatayu. Koma iye apite
pamodzi ndi abale akewa. 34 Ndingabwerere bwanji kwa abambo anga
ngati sindingapite ndi mnyamatayu? Ayi! Sindifuna kukaona tsoka limene
lingakagwere abambo anga.”

# 45

*Yosefe Adziwulula kwa Abale Ake*

[1] Tsono Yosefe sanathenso kuwugwira mtima kuti asalire pamaso pa
antchito ake ndipo anafuwula kuti, “Aliyense achoke pamaso panga!”
Motero panalibe wina aliyense pamene Yosefe anadziwulula kwa abale
ake. [2] Ndipo analira mokweza mwakuti Aigupto anamva. Onse a ku
nyumba kwa Farao anamvanso za zimenezi.
[3] Yosefe anati kwa abale ake, “Ine ndine Yosefe! Kodi abambo anga
akanali ndi moyo?” Koma abale ake sanathe kumuyankha chifukwa anali
ndi mantha kwambiri pamaso pake.
[4] Ndipo Yosefe anati kwa abale ake, “Senderani pafupi nane.”
Atasendera iye anati, “Ine ndine m’bale wanu Yosefe amene muna-
mugulitsa ku Igupto! [5] Ndipo tsopano, musawawidwe mtima kapena
kudzipsera mtima chifukwa choti munandigulitsa ine kuno, popeza
Mulungu ananditsogoza ine kuti adzapulumutse miyoyo yanu. [6] Kwa
zaka ziwiri tsopano, kwakhala kuli njala m’dziko muno, ndipo kwa zaka
zisanu zikubwerazi, anthu sadzalima kapena kukolola. [7] Koma Mulungu
ananditsogoza kuti adzakusungeni ndi moyo ndi kuti mudzakhale ndi
zidzukulu pa dziko lapansi.
[8] “Motero, si inu amene munanditumiza kuno koma Mulungu. Iye anan-
disandutsa kukhala nduna yayikulu ya Farao, ndipo zonse za m’nyumba
mwake zili m’manja mwangamu. Komanso amene akulamulira dziko
lonse la Igupto ndi ine. [9] Tsono fulumirani mubwerere kwa abambo
anga ndi kuwawuza kuti, ‘Mwana wanu Yosefe akuti, Mulungu anan-
disandutsa kukhala mbuye wa dziko lonse la Igupto. Ndiye bwerani kuno
musachedwe. [10] Ndipo inu, ana anu, zidzukulu zanu, pamodzi ndi nkhosa
ndi ng’ombe zanu ndi antchito anu amene muli nawo muzidzakhala
m’dziko la Goseni pafupi ndi ine. [11] Ine ndizidzakupatsani zakudya
kumeneko chifukwa zaka zisanu za njala zikubwera ndithu. Kupanda
kutero, inu ndi mabanja anu pamodzi ndi anthu anu onse mudzasowa
chakudya.’
[12] “Tsono inu nonse pamodzi ndi m’bale wangayu Benjamini, mukuona
kuti ndi inedi amene ndikuyankhula nanu. [13] Mukawawuze abambo
anga kuti ndili pa ulemerero ku dziko la Igupto kuno ndi zonse zimene
mwaziona. Tsopano fulumirani kuti mukabwere nawo kuno abambo
anga.”
[14] Kenaka Yosefe anakhumbatira Benjamini, mng’ono wake uja
nayamba kulira. Nayenso Benjamini anayamba kulira atamukumbatira.
[15] Atatero, Yosefe anapsompsona abale ake onse aja, akulira. Pambuyo
pake abale ake aja anacheza ndi Yosefe.
[16] Akunyumba kwa Farao atamva kuti abale ake a Yosefe abwera,
Farao pamodzi ndi nduna zake zonse anakondwera. [17] Farao anati kwa
Yosefe, “Uwawuze abale ako kuti, ‘Senzetsani nyama zanu katundu ndi
kubwerera ku dziko la Kanaani. [18] Mukabwere nawo abambo anu ndi
mabanja anu kuno, ndipo ine ndidzakupatsani dera lachonde kwambiri
m’dziko la Igupto. Mudzadya zokoma za m’dzikoli.’ ”
[19] “Uwawuzenso kuti, ‘Tengani ngolo zingapo za kuno ku Igupto kuti
mukakwezepo ana anu, akazi anu pamodzi ndi abambo ako ndi kubwera
nawo kuno. [20] Musadandaule zosiya katundu komweko chifukwa dziko
lachonde la kuno ku Igupto lidzakhala lanu.’ ”
[21] Choncho ana a Israeli anachita zimenezo. Yosefe anawapatsa ngolo
monga Farao analamulira, ndipo anawapatsanso chakudya cha paulendo
wawo. [22] Anaperekanso kwa aliyense zovala zatsopano, koma kwa

Benjamini anapereka siliva wolemera pafupifupi makilogalamu anayi ndi
zovala zisanu. 23 Ndipo abambo ake anawatumizira izi: abulu khumi
osenza zinthu zabwino kwambiri za ku Igupto, ndi abulu aakazi khumi
osenza tirigu, buledi ndi zakudya zina za pa ulendo wake. 24 Kenaka
anawalola abale ake aja kuti azipita, ndipo akunyamuka, iye anawawuza
kuti, "Osakangana m'njira!"

25 Ndipo anachoka ku Igupto nafika kwa abambo awo Yakobo m'dziko
la Kanaani. 26 Iwo anawuza abambo awo kuti, "Yosefe akanali ndi
moyo! Ndiponsotu, ndiye akulamulira dziko la Igupto." Yakobo anangoti
kakasi osankhulupirira. 27 Komabe atamufotokozera zonse zimene Yosefe
anawawuza ndipo ataona ngolo zimene Yosefe anatumiza kuti adzakw-
eremo popita ku Igupto, mtima wa Yakobo, abambo awo unatsitsimuka.
28 Ndipo Israeli anati, "Ndatsimikizadi! Mwana wanga Yosefe akanali ndi
moyodi. Ndipita ndikamuone ndisanafe."

# 46

### *Yakobo Apita ku Igupto*

1 Israeli anasonkhanitsa zonse anali nazo napita ku Beeriseba
kukapereka nsembe kwa Mulungu wa abambo ake Isake.

2 Ndipo Mulungu anayankhula ndi Israeli m'masomphenya usiku nati,
"Yakobo! Yakobo!"

Iye anayankha, "Ee, Ambuye."

3 Mulungu anati, "Ine ndine Mulungu. Mulungu wa abambo ako.
Usachite mantha kupita ku Igupto, pakuti ndidzachulukitsa zidzukulu zako
kumeneko moti zidzakhala mtundu waukulu. 4 Ine ndidzapita ku Igupto
pamodzi ndi iwe ndipo mosakayika konse zidzukulu zako ndidzazibw-
eretsa konkuno. Yosefe adzakhalapo pa nthawi yako yomwalira."

5 Yakobo anachoka ku Beeriseba, ndipo ana ake anakweza abambo awo,
ana awo, pamodzi ndi akazi awo pa ngolo zimene Farao anatumiza kuti
adzakwerepo. 6 Iwo anatenganso ziweto zawo ndi katundu wawo amene
anali naye ku Kanaani, ndipo Yakobo pamodzi ndi ana ndi zidzukulu zake
anapita ku Igupto. 7 Ndiye kuti popita ku Igupto Yakobo anatenga ana
aamuna, zidzukulu zazimuna, ana aakazi ndi zidzukulu zazikazi.

8 Nawa ana a Israeli (ndiye kuti Yakobo ndi ana ake) amene anapita ku
Igupto:

Rubeni mwana woyamba wa Yakobo.

9 Ana aamuna a Rubeni ndi awa:
Hanoki, Palu, Hezironi ndi Karimi.

10 Ana aamuna a Simeoni ndi awa:
Yemueli, Yamini, Ohadi, Yakini, Zohari ndi Shaulo amene mayi wake anali wa ku Kanaani.

11 Ana aamuna a Levi ndi awa:
Geresoni, Kohati ndi Merari.

12 Ana aamuna a Yuda ndi awa:
Eri, Onani, Sela, Perezi ndi Zera. Koma Eri ndi Onani anamwalira m'dziko la Kanaani.
Ana a Perezi anali
Hezironi ndi Hamuli.

13 Ana aamuna a Isakara ndi awa:
Tola, Puwa, Yobi ndi Simironi.

14 Ana aamuna a Zebuloni ndi awa:
Seredi, Eloni ndi Yahaleeli.
15 Amenewa ndi ana aamuna a Leya amene anamubalira Yakobo ku Padanaramu. Panali mwana wamkazi dzina lake Dina. Ana onse analipo 33.

16 Ana aamuna a Gadi ndi awa:
Zifioni, Hagi, Suni, Eziboni, Eri, Arodi ndi Areli.
17 Ana aamuna a Aseri ndi awa:
Imuna, Isiva, Isivi, Beriya
ndi Sera mlongo wawo.
Ana aamuna a Beriya ndi awa:
Heberi ndi Malikieli.
18 Amenewa ndi zidzukulu za Yakobo mwa Zilipa amene Labani anapereka kwa mwana wake, Leya. Onse pamodzi analipo 16.

19 Ana aamuna a Rakele mkazi wa Yakobo anali:
Yosefe ndi Benjamini. 20 Ku Igupto, Asenati mwana wa Potifara
wansembe wa Oni, anamuberekera Yosefe ana awa: Manase ndi Efereimu.
21 Ana aamuna a Benjamini ndi awa:
Bela, Bekeri, Asibeli, Gera, Naamani, Ehi, Rosi, Mupimu, Hupimu ndi Aridi.
22 Amenewa ndi zidzukulu za Yakobo mwa mkazi wake Rakele. Onse analipo khumi ndi anayi.

23 Mwana wa mwamuna wa Dani anali:
Husimu.
24 Ana aamuna a Nafutali ndi awa:
Yahazeeli, Guni, Yezeri ndi Silemu.
25 Amenewa ndi zidzukulu za Yakobo mwa Biliha amene Labani anapereka kwa mwana wake Rakele. Onse pamodzi analipo asanu ndi awiri.

26 Onse amene anapita ndi Yakobo (iwo amene anali akeake, osaw-
erengera akazi a ana ake), analipo 66. 27 Pophatikiza ana awiri a Yosefe
obadwira ku Igupto, anthu a pa banja la Yakobo amene anapita ku Igupto, onse pamodzi analipo 70.

28 Tsopano Yakobo anatumiza Yuda kwa Yosefe kukamupempha kuti
akakumane naye ku Goseni. Iwo atafika ku chigawo cha Goseni,
29 Yosefe anakonza galeta nakwerapo ndi kupita ku Goseni kukakumana
ndi abambo ake, Israeli. Yosefe atangofika pamaso pa abambo ake, anawakumbatira nalira kwa nthawi yayitali.
30 Israeli anati kwa Yosefe, “Tsopano ndikhoza kumwalira poti ndaona nkhope yako kuti ukanali ndi moyo.”
31 Ndipo Yosefe anati kwa abale ake pamodzi ndi a pa banja la abambo
ake, “Ndipita kwa Farao ndipo ndikamuwuza kuti, ‘Abale anga pamodzi
ndi onse a m’nyumba ya abambo anga amene amakhala m’dziko la
Kanaani abwera kuno kwa ine. 32 Anthuwa ndi abusa; amaweta ziweto
zawo ndipo abwera ndi nkhosa ndi ng’ombe zawo, pamodzi ndi antchito
awo.’ 33 Tsono Farao akakuyitanani nakufunsani kuti, ‘Kodi mumagwira
ntchito yanji?’ 34 Muyankhe kuti, ‘Ife, bwana ndife oweta ziweto

kuyambira ubwana wathu mpaka tsopano. Takhala tikuweta ziweto
monga mmene ankachitira makolo athu.' Mukadzayankha choncho,
ndiye kuti mudzakhala m'dziko la Goseni chifukwa anthu a ku Igupto
amanyansidwa nawo anthu oweta ziweto."

# 47

1 Yosefe anapita kukamuwuza Farao kuti, "Abambo anga, abale anga
pamodzi ndi nkhosa, ng'ombe zawo, ndi antchito awo abwera kuchokera
ku dziko la Kanaani ndipo tsopano ali ku Goseni." 2 Iye anapita kwa Farao
kuja ndi abale ake asanu, kukawaonetsa.

3 Farao anafunsa abale akewo kuti, "Mumagwira ntchito yanji?"

Iwo anamuyankha kuti, "Ife, bwana ndife oweta ziweto, monga ankachi-
tira makolo athu. 4 Ife tabwera kudzakhala kuno kwa kanthawi chifukwa
njala yafika poopsa ku Kanaani motero kuti kulibe msipu wodyetsera
ziweto. Ndiye bwana tiloleni kuti tikhale ku Goseni."

5 Farao anati kwa Yosefe, "Abambo ako ndi abale ako abwera kwa
iwe. 6 Dziko lonse la Igupto lili m'dzanja lako. Uwakhazike abambo
ako ndi abale ako m'malo achonde kwambiri. Akhale ku Goseni. Ndipo
ngati ukudziwapo ena mwa iwo amene ali akatswiri pa kuweta ziweto,
uwapatse udindo woyang'anira ziweto zanga."

7 Kenaka Yosefe anapita ndi abambo ake kwa Farao kukawaonetsa,
ndipo Yakobo anadalitsa Faraoyo. 8 Atatero, Farao anafunsa Yakobo kuti,
"Muli ndi zaka zingati?"

9 Yakobo anayankha kuti, "Zaka za maulendo anga zakwana 130. Zaka
za moyo wanga ndi zowerengeka, komanso zakhala zaka za masautso.
Zaka za moyo wanga sizingafanane ndi zaka za moyo wa makolo anga."
10 Atatha kumudalitsa Farao uja, Yakobo anatsanzika n'kunyamuka.

11 Choncho Yosefe anakhazika abambo ake aja ndi abale ake m'dziko
la Igupto. Iye anawapatsa dera la Ramesesi limene linali dziko lachonde
kwambiri monga analamulira Farao. 12 Yosefe anaperekanso chakudya
kwa abambo ake, kwa abale ake ndi kwa onse a m'nyumba ya abambo
ake monga mwa chiwerengero cha ana awo.

### *Yosefe pa Nthawi ya Njala*

13 Njala inakula kwambiri motero kuti chakudya chinasowa m'dziko
lonse. Anthu a ku Igupto ndi ku Kanaani analefuka nayo njalayo. 14 Yosefe
anasonkhanitsa ndalama zonse zimene anthu a mu Igupto ndi Kanaani
ankapereka pogula tirigu, ndipo anabwera nazo ku nyumba kwa Farao.
15 Anthu a ku Igupto ndi Kanaani ndalama zitawathera, Aigupto onse
anabwera kwa Yosefe nati, "Tipatseni chakudya. Nanga tiferenji pamaso
panu? Ndalama zathu zatha."

16 Ndipo Yosefe anawayankha kuti, "Bwerani ndi ziweto zanu ndipo
tidzasinthana ndi chakudya poti mukuti ndalama zanu zatha." 17 Choncho
anthu anabwera ndi ziweto zawo monga akavalo, nkhosa, mbuzi, ng'ombe
ndi abulu ndipo Yosefe anawapatsa zakudya.

18 Chitatha chaka chimenecho, anthu anapitanso kwa Yosefe chaka
chinacho nati, "Ife sitingakubisireni mbuye wathu kuti ndalama zathu
zatithera ndipo ziweto zathu zili ndi inu, palibenso choti n'kukupatsani
mbuye wathu kupatula matupi athu ndi dziko lathu. 19 Tiferenji ife ndi
dziko lathu inu mukuona? Mutipatse chakudya ndipo tidzigulitsa ife ndi

minda yathu yomwe. Ife tidzakhala akapolo a Farao. Tipatseni mbewuzo kuti tikhale ndi moyo tisafe ndipo dziko lisachite bwinja.”

20 Choncho Yosefe anamugulira Farao dziko lonse la Igupto. Aliyense mu
Igupto anagulitsa munda wake chifukwa njala inakula kwambiri. Dziko
lonse linasanduka la Farao, 21 ndipo Yosefe anawasandutsa anthu onse
kukhala akapolo a Farao, kuchokera ku malire a mbali ina ya Igupto
kukafika ku malire a mbali ina ya dzikolo. 22 Komabe, sanagule minda ya
ansembe chifukwa Farao ankawapatsa thandizo lokwanira. N'chifukwa
chake sanagulitse minda yawo.

23 Yosefe anati kwa anthuwo, “Tsono poti ndakugulani inu ndi minda
yanu, kugulira Farao. Nayi mbewu kuti mudzale m'minda yanu. 24 Koma
podzakolola, mudzapereka gawo limodzi la magawo asanu aliwonse kwa
Farao. Magawo anayi enawo adzakhala anu. Zina mudzasunge mbewu
ndi zina mudzadye inuyo, mabanja anu ndi ana anu.”

25 Iwo anati, “Mwatipulumutsa potichitira zabwinozi, mbuye wathu,
tsono tidzakhala akapolo a Farao.”

26 Choncho Yosefe anakhazikitsa lamulo limene lilipobe mpaka lero
m'dziko lonse la Igupto kuti limodzi la magawo asanu a zokolola ndi la
Farao. Ndi minda ya ansembe yokha imene sinatengedwe kukhala ya
Farao.

27 Tsono Aisraeli anakhazikika m'dziko la Igupto ku chigawo cha Goseni.
Kumeneko anapeza chuma ndipo anaberekana nachuluka kwambiri.

28 Yakobo anakhala ku Igupto zaka 17 ndipo zaka za moyo wake zinali
147. 29 Nthawi itayandikira yoti Israeli amwalire, anayitanitsa mwana
wake Yosefe nati kwa iye, “Ngati ukundikondadi monga abambo ako,
ika dzanja lako pansi pa ntchafu yanga ndipo ulonjeze kuti udzaonetsa
kukoma mtima ndi kukhulupirika kwako kwa ine kuti sudzayika mtembo
wanga kuno ku Igupto. 30 Ine ndikagona pamodzi ndi makolo anga.
Choncho ndikadzamwalira udzanditulutse mu Igupto muno ndipo ukayike
mtembo wanga kumene anayikidwa makolo anga.”

Yosefe anati, “Ndidzachita monga mwanenera.”

31 Yakobo anati, “Lumbira kwa ine.” Yosefe analumbira kwa iye, ndipo
Israeli anapembedza Mulungu atatsamira ndodo yake.

# 48

*Manase ndi Efereimu*

1 Patapita kanthawi Yosefe anawuzidwa kuti, “Abambo ako akudwala.”
Choncho anatenga ana ake awiri aja Manase ndi Efereimu ndi kupita nawo
kwa Yakobo. 2 Yakobo atawuzidwa kuti, “Mwana wanu Yosefe wabwera,”
Israeli anadzilimbitsa nadzuka kukhala tsonga pa bedi pake.

3 Yakobo anati kwa Yosefe, “Mulungu Wamphamvuzonse anandionekera
ku Luzi m'dziko la Kanaani, ndipo anandidalitsa, 4 nati kwa ine, ‘Ndidza-
kupatsa ana ambiri ndipo zidzukulu zako zidzasanduka mitundu yambiri
ya anthu. Ndidzapereka dziko ili kwa zidzukulu zako zobwera pambuyo
pako kuti likhale lawo mpaka muyaya.’

5 “Tsopano ana ako aamuna awiri amene anabadwa ine ndisanabwere
kuno adzakhala ana anga. Efereimu ndi Manase adzakhala anga monga
mmene alili Rubeni ndi Simeoni. 6 Koma amene ati adzabadwe pambuyo
pa iwowa adzakhala ako ndipo cholowa chawo chidzadziwika ndi mayina
a abale awo. 7 Pamene ndimabwerera kuchoka ku Parani, mwachisoni

Rakele, amayi ako anamwalira m'dziko la Kanaani, tikanali m'njira,
mtunda wokafika ku Efurata ukanalipo. Ndipo ndinawayika kumeneko
m'mphepete mwa msewu wa ku Efurata" (amene ndi Betelehemu).
8 Israeli ataona ana a Yosefe anafunsa kuti, "Anyamatawa ndi a yani?"
9 Yosefe anati kwa abambo ake, "Awa ndi ana anga amene Mulungu
wandipatsa kuno."

Ndipo Israeli anati, "Bwera nawo kuno kuti ndiwadalitse."
10 Koma maso a Israeli anali ofowoka chifukwa cha kukalamba moti
sankaona n'komwe. Tsono Yosefe anabwera nawo ana ake aja pafupi ndi
abambo ake ndipo abambo ake anawapsompsona nawakumbatira.
11 Israeli anati kwa Yosefe, "Ine sindinali kuyembekeza kuti
n'kudzaonanso nkhope yako, ndipo tsopano Mulungu wandilola kuti
ndionenso ngakhale ana ako."
12 Tsono Yosefe anawachotsa ana aja pa mawondo a Israeli ndipo
anamuweramira nkhope pansi. 13 Yosefe anawagwira ana onse awiri
padzanja, Efereimu ku dzanja lake lamanja kulunjika dzanja lamanzere la
Israeli ndipo Manase ku dzanja lamanzere kulunjikitsa dzanja lamanja la
Israeli, ndipo anawayandikiza kwa Yakobo. 14 Koma Israeli anapinganitsa
mikono motero kuti anayika dzanja lake lamanja pamutu pa Efereimu
ngakhale kuti iyeyo anali wamng'ono ndi dzanja lake lakumanzere
analisanjika pamutu pa Manase ngakhale kuti iyeyu ndiye anali mwana
woyamba.
15 Kenaka anadalitsa Yosefe nati,

"Mulungu amene makolo anga
Abrahamu ndi Isake anamutumikira,
Mulungu amene wakhala ali m'busa wanga
moyo wanga wonse kufikira lero,
16 mngelo amene wandipulumutsa ine ku zovuta zonse,
ameneyo adalitse anyamata awa.
Kudzera mwa iwowa
dzina langa ndi mayina a makolo anga, Abrahamu ndi Isake, adzamveka.
Iwowa adzakhala ndi ana ambiri nadzasanduka mtundu waukulu
pa dziko lapansi."

17 Yosefe ataona kuti abambo ake ayika dzanja lamanja pa Efereimu,
sanakondwere. Choncho anagwira dzanja la abambo ake kuti alichotse
pamutu pa Efereimu ndi kuliyika pamutu pa Manase, 18 nati kwa abambo
ake, "Ayi, abambo anga, uyu ndiye woyamba kubadwa, ikani dzanja lanu
lamanja pamutu pake."
19 Koma abambo ake anakana nati, "Ndikudziwa, mwana wanga,
ndikudziwa. Adzukulu a iyeyunso adzakhala mtundu waukulu. Komabe
m'bale wake wamng'onoyu adzakhala wamkulu kuposa iye, ndipo
zidzukulu zake zidzakhala mitundu yayikulu ya anthu." 20 Tsono iye
anawadalitsa tsiku limenelo nati,

"Aisraeli adzagwiritsa ntchito dzina lanu podalitsa nadzati:
Mulungu akudalitseni monga Efereimu ndi Manase."

Choncho anayika Efereimu patsogolo pa Manase.
21 Kenaka Israeli anati kwa Yosefe, "Ine ndatsala pang'ono kufa, koma
Mulungu adzakhala ndipo adzakutenganinso kubwerera nanu ku dziko la
makolo anu. 22 Ndiponso iwe wekha ndikupatsa moposera abale ako, malo
woonjezera, Sekemu, malo amene ndinalanda kwa Aamori ndi lupanga
ndi uta wanga."

# 49

### *Yakobo Adalitsa Ana ake Aamuna*

1 Pambuyo pake Yakobo anayitanitsa ana ake aamuna nati: Sonkhanani
pamodzi kuti ndikuwuzeni zimene zidzakuchitikireni m'masiku a
m'tsogolo.

2 "Bwerani ndipo imvani mawu anga, inu ana a Yakobo;
mverani abambo anu Israeli.

3 "Rubeni, ndiwe woyamba kubadwa;
mphamvu yanga ndiponso chizindikiro choyamba cha mphamvu zanga,
wopambana pa ulemerero ndi mphamvu.
4 Wokokoma ngati madzi a chigumula, koma sudzakhalanso wopambana,
iwe unagona pa bedi la abambo ako,
ndithu unayipitsa bedi la mdzakazi wake.

5 "Simeoni ndi Levi ndi pachibale pawo,
anachitira nkhanza anthu amene anachita nawo pangano.
6 Iwe moyo wanga, usakhale nawo pa misonkhano yawo ya mseri,
kapena kugwirizana nawo m'mabwalo awo,
pakuti anapha anthu mu mkwiyo wawo
ndipo anapundula ng'ombe zamphongo monga kunawakomera.
7 Matemberero awagwere chifukwa cha mkwiyo wawo woopsa chonchi
ndi ukali wawo wankhanza choterewu!
Ine ndidzawabalalitsa m'dziko la Yakobo
ndi kuwamwaza iwo m'dziko la Israeli.

8 "Yuda, ndiwe amene abale ako adzatamanda;
dzanja lako lidzagwira pa khosi pa adani ako;
abale ako adzakugwadira iwe.
9 Yuda ali ngati mwana wa mkango;
umabwerera ku malo ako ndi zofunkha, mwana wanga.
Monga mkango, amadziwongola ndi kugona pansi,
ndipo ngati mkango waukazi, ndani angalimbe mtima kumudzutsa?
10 Ndodo yaufumu sidzachoka mwa Yuda,
udzawupanirira ulamuliro motero kuti palibe amene adzawuchotse,
mpaka mwini wake weniweni atabwera
ndipo mitundu yonse ya anthu idzamumvera.
11 Ndiye amene amamangirira bulu wake wamkazi kumtengo wa mpesa,
ndi mwana wa bulu ku nthambi ya mpesa wabwino.
Ndi iye amene amachapa zovala zake mu vinyo;
ndi mkanjo wake mu vinyo wofiira ngati magazi.
12 Maso ake adzakhala akuda chifukwa cha vinyo,
mano ake woyera chifukwa cha mkaka.

13 "Zebuloni adzakhala m'mphepete mwa nyanja;
adzakhala pa dooko la sitima zapamadzi;
malire ake adzafika ku Sidoni.

14 "Isakara ali ngati bulu wamphamvu
wogona pansi pakati pa makola.
15 Ataona ubwino wake wa pamalo pake popumira

ndi kukongola kwa dziko lake,
iye anaweramutsa msana kuti anyamule katundu wake
ndipo anasanduka wogwira ntchito ya ukapolo.

16 “Dani adzaweruza mwachilungamo anthu ake
monga limodzi mwa mafuko a anthu a mu Israeli.
17 Dani adzakhala ngati njoka ya m’mphepete mwa msewu,
songo yokhala m’njira
imene imaluma chidendene cha kavalo
kuti wokwerapoyo agwe chagada.

18 “Ndikuyembekeza chipulumutso chanu Yehova.

19 “Gadi adzachitidwa chiwembu ndi gulu la amaliwongo,
koma iye adzawathamangitsa.

20 “Dziko la Aseri lidzabereka chakudya chokoma,
ndipo iye adzapereka chakudya kwa mafumu.

21 “Nafutali ali ngati mbawala yayikazi
yokhala ndi ana okongola kwambiri.

22 “Yosefe ali ngati mtengo wobereka zipatso,
mtengo wobereka zipatso pafupi ndi kasupe,
nthambi zake zimayanga pa chipupa cha mwala.
23 Alenje a uta anamuchita chiwembu mwankhanza;
anamuthamangitsa ndi mauta awo.
24 Koma uta wake sunagwedezeke,
ndi manja ake amphamvu aja analimbika,
chifukwa cha mphamvu za Mulungu Wamphamvu wa Yakobo,
chifukwa ali M’busa ndi Thanthwe la Israeli.
25 Chifukwa cha Mulungu wa makolo ako amene amakuthandiza;
chifukwa cha Mulungu Wamphamvu, amene amakudalitsa
ndi mvula yochokera kumwamba,
ndi madzi otumphuka pansi pa nthaka,
ndipo amakudalitsa pokupatsa ana ambiri ndi ng’ombe zambiri.
26 Madalitso a kholo lako ndi amphamvu kuposa
madalitso a mapiri akale
oposa zabwino za ku zitunda zamgonagona.
Zonse izi zikhale pamutu pa Yosefe,
pa mphumi pa wopatulika uja amene anapatulidwa pakati pa abale ake.

27 “Benjamini ali ngati m’mbulu wolusa;
umene mmawa umapha ndi kudya zofunkha,
ndipo madzulo umagawa zofunkhazo,”

28 Onse awa ndi mafuko khumi ndi awiri a Israeli, ndipo zimenezi ndi zomwe abambo awo ananena pamene anawadalitsa, kuwapatsa aliyense madalitso ake womuyenera iye.

### *Kumwalira kwa Yakobo*

29 Kenaka Yakobo analamula ana ake nati: “Ine ndatsala pang’ono kufa.
Tsono mukandiyike pamodzi ndi makolo anga m’phanga la m’munda wa
Efroni Mhiti. 30 Ili ndi phanga la m’munda wa Makipela, pafupi ndi
Mamre m’dziko la Kanaani. Abrahamu anagula phangalo pamodzi ndi
munda womwe kwa Efroni Mhiti kuti pakhale manda. 31 Kumeneko
kunayikidwa Abrahamu ndi mkazi wake Sara, Isake ndi mkazi wake
Rebeka ndipo ndinayikakonso Leya. 32 Munda ndi manda amene ali
m’menemo zinagulidwa kwa Ahiti.”

33 Yakobo atamaliza kupereka malangizo kwa ana ake, anabwezera
miyendo yake pa bedi, namwalira ndipo anakakhala ndi anthu a mtundu
wake.

# 50

1 Kenaka Yosefe anadzigwetsa pa nkhope ya abambo ake, nawap-
sompsona kwinaku akulira. 2 Ndipo Yosefe analamula antchito ake a
chipatala kuti akonze thupi la Israeli ndi mankhwala kuti lisawole. Kotero
antchitowo anakonzadi thupilo. 3 Antchito aja zinawatengera masiku 40
kuti akonze mtembo uja popeza ntchito ngati imeneyi inafunikira masiku
monga amenewa. Ndipo Aigupto anamulira Yakobo kwa masiku makumi
asanu ndi awiri.

4 Yosefe atatha kulira maliro a abambo ake, anayankhula kwa nduna
za Farao nati, “Ngati mungandikomere mtima, chonde mundiyankhulire
kwa Farao kumuwuza kuti, 5 ‘Abambo anga anandilumbiritsa ndipo anati,
‘Ndatsala pang’ono kumwalira, ukandiyike m’manda amene ndinakumba
ndekha m’dziko la Kanaani.’ Tsono mundilole ndikayike abambo anga,
ndipo ndikabweranso.’ ”

6 Farao anati, “Pita ukayike abambo ako monga anakulumbiritsa kuti
uchite.”

7 Kotero Yosefe anapita kukayika abambo ake. Nduna zonse za Farao,
akuluakulu a bwalo lake ndi akuluakulu a ku Igupto, anapita naye
pamodzi. 8 Anapitanso onse a pa banja la Yosefe ndi abale ake ndi onse
amene anali a pa banja la abambo ake. Ana awo okha, nkhosa ndi
ng’ombe zinatsala ku Goseni 9 Asilikali okwera pa magaleta ndi asilikali a
pa akavalo anapita nayenso pamodzi. Linali gulu lalikulu.

10 Atafika pa Goreni ha-Atadi, pafupi ndi Yorodani, anachita mwambo
waukulu wa maliro. Choncho Yosefe analira maliro a abambo ake masiku
asanu ndi awiri. 11 Akanaani amene ankakhala ku Goreni ha-Atadi ataona
mwambo wa maliro anati, “Aigupto ali ndi mwambo wa maliro a akulu.”
Ndi chifukwa chake malo amenewo a pafupi ndi Yorodani amatchedwa
Abeli-Mizraimu.

12 Choncho ana a Yakobo anachita monga momwe abambo awo
anawalamula: 13 Ndiye kuti ana a Yakobo anamunyamula kupita naye
ku Kanaani kuti akamuyike m’phanga limene lili m’munda wa Makipela
pafupi ndi Mamre. Abrahamu anagula mundawo kwa Efroni Mhiti kuti
pakhale manda. 14 Atatha kuyika abambo ake, Yosefe anabwerera ku
Igupto, pamodzi ndi abale ake ndi onse amene anapita nawo kukayika
abambo ake.

### *Yosefe Abwereza Kutsimikizira Abale Ake*

15 Abale ake a Yosefe ataona kuti abambo awo amwalira, anati, “Nanga
tidzatani ngati Yosefe anatisungira mangawa nafuna kutibwezera pa
zoyipa zonse zimene tinamuchitira?” 16 Motero anatumiza mawu kwa

Yosefe kuti, “Abambo anu anasiya malangizo asanafe nati: 17 ‘Zimene
mudzayenera kunena kwa Yosefe ndi izi: Ndikukupempha kuti uwakhulu-
lukire abale ako cholakwa chawo ndi machimo awo, popeza anakuchitira
zoyipa.’ Ndiye tsopano chonde tikhululukireni zolakwa zimene ife
akapolo a Mulungu wa abambo anu tinachita.” Yosefe atangomva mawu
amenewa anayamba kulira.

18 Kenaka abale ake anabwera nadzigwetsa pansi pamaso pake, nati, “Ife
ndife akapolo anu.”

19 Koma Yosefe anawawuza kuti, “Musachite mantha. Kodi ine ndalowa
m’malo mwa Mulungu? 20 Inu munafuna kundichitira zoyipa, koma
Mulungu anasandutsa zoyipazo kuti zikhale zabwino kuti zikwaniritsidwe
zimene zikuchitika panozi, zopulumutsa miyoyo yambiri. 21 Kotero,
musachite mantha. Ine ndidzasamalira inu pamodzi ndi ana anu omwe.”
Tsono iye anawalimbitsa mtima powayankhula moleza mtima.

### *Kumwalira kwa Yosefe*

22 Yosefe anakhala mu Igupto pamodzi ndi banja lonse la abambo ake.
Anakhala ndi moyo zaka 110 23 ndipo anaona m’bado wachitatu wa ana a
Efereimu. Yosefe anatenganso ana a Makiri, mwana wa Manase kukhala
ngati ana a m’banja lake.

24 Kenaka Yosefe anati kwa abale ake, “Ine ndatsala pang’ono kufa.
Koma mosakayika Mulungu adzakuyang’anirani nadzakutengani kukutu-
lutsani m’dziko lino kupita ku dziko limene Iye analonjeza kwa Abrahamu,
Isake ndi Yakobo.” 25 Ndipo Yosefe analumbiritsa ana a Israeli lumbiro
nati, “Lonjezani kuti Mulungu akadzakusungani mudzanyamula mafupa
anga kuwachotsa ku malo kuno.”

26 Choncho Yosefe anafa ali ndi zaka 110. Motero iwo atakonza thupi
lake ndi mankhwala kuti lisawole, analiyika m’bokosi ku Igupto.

# Eksodo

### *Aisraeli Azunzidwa ku Igupto*

1 Awa ndi mayina a ana a Israeli amene anapita ku Igupto pamodzi ndi
Yakobo abambo awo, aliyense ndi banja lake: 2 Rubeni, Simeoni, Levi,
Yuda; 3 Isakara, Zebuloni, Benjamini; 4 Dani, Nafutali; Gadi ndi Aseri.
5 Anthu onse obadwa mwa Yakobo analipo 70. Yosefe n'kuti ali kale ku
Igupto.

6 Tsono Yosefe ndi abale ake onse ndiponso m'bado wawo wonse
anamwalira. 7 Koma Aisraeli anaberekana ndi kuchuluka kwambiri
nakhala amphamvu kwambiri, kotero kuti anadzaza dzikolo.

8 Pambuyo pake mfumu yatsopano imene sinkamudziwa Yosefe, in-
ayamba kulamulira dziko la Igupto. 9 Iyo inati kwa anthu ake, "Taonani,
Aisraeli achuluka ndipo ndi amphamvu kwambiri kuposa ife. 10 Tiyeni
tiwachenjerere. Tikapanda kutero adzachuluka kuposa ife, ndipo ngati
kutakhala nkhondo, adzadziphatika kwa adani athu nadzamenyana nafe,
kenaka n'kudzachoka m'dziko muno."

11 Kotero anayika akapitawo kuti aziwazunza ndi kuwagwiritsa ntchito
yolemetsa mokakamiza. Iwo anamangira Farao mizinda ya Pitomu
ndi Ramesesi kumene ankasungirako chakudya. 12 Koma pamene
ankawazunza kwambiri, Aisraeli ndiye ankachulukirachulukira mpaka
kubalalikira m'dziko lonse. Kotero Aigupto anayamba kuopa Aisraeliwo
13 ndipo anawagwiritsa ntchito mwankhanza kwambiri. 14 Aigupto
anachititsa moyo wa Aisraeli kukhala owawa kwambiri powagwiritsa
ntchito yakalavulagaga yowumba njerwa ndi kuponda dothi lomangira,
pamodzi ndi ntchito zina zosiyanasiyana zam'minda. Iwo anakakamiza
Aisraeli mwankhanza kuti agwire ntchito yowawayi.

### *Azamba Akana Kumvera Mfumu*

15 Mfumu ya Igupto inati kwa azamba a Chihebri omwe mayina awo
anali Sifira ndi Puwa, 16 "Mukamathandiza amayi a Chihebri pa mwala
wochirira, muzionetsetsa kuti akabadwa mwana wamwamuna muzipha,
koma akakhala wamkazi muzimuleka akhale ndi moyo." 17 Koma
azambawo ankaopa Mulungu ndipo sanachite zimene mfumu ya Igupto
inawawuza kuti achite. Iwo analeka ana aamuna kuti akhale ndi moyo.
18 Kenaka mfumu ya Igupto inayitanitsa azamba aja ndi kuwafunsa kuti,
"Chifukwa chiyani mwachita zimenezi? Bwanji mwasiya ana aamuna kuti
akhale ndi moyo?"

19 Azambawo anamuyankha Farao kuti, "Amayi a Chihebri sali
ngati amayi a Chiigupto; Iwo ndi amphamvu ndipo amachira azamba
asanafike."

20 Kotero Mulungu anawakomera mtima azambawo, ndipo Aisraeli
anapitirirabe kuchulukana nakhala amphamvu kwambiri. 21 Pakuti
azambawo ankaopa Mulungu, Iye anawapatsa mabanja awoawo.

22 Pamenepo Farao analamulira anthu ake onse kuti, "Mwana wamwa-
muna aliyense akabadwa, mukamuponye mu mtsinje wa Nailo, koma
wamkazi mulekeni akhale ndi moyo."

# 2

*Kubadwa kwa Mose*

1 Ndipo munthu wina wa fuko la Levi anakwatira mkazi wa fuko
lomwelo. 2 Mkaziyo anatenga pathupi ndipo anabereka mwana wamwa-
muna. Ataona kuti mwanayo anali wokongola, anamubisa kwa miyezi
itatu. 3 Koma mwanayo atafika pa msinkhu woti sakanathanso kubisidwa,
amayi ake anatenga kadengu kopangidwa ndi bango nakamata phula.
Kenaka anayika mwanayo m'menemo ndi kukamuyika pa mabango mu
mtsinje wa Nailo. 4 Mlongo wake wa mwanayo anayima pataliko kuti aone
chimene chidzamuchitikira mwanayo.

5 Mwana wamkazi wa Farao anapita ku mtsinje wa Nailo kukasamba
ndipo adzakazi ake ankayenda m'mbali mwa mtsinjewo. Tsono mwana
wa Farao uja anaona kadenguko pakati pa mabango ndipo anatuma
mdzakazi wake kuti akakatenge. 6 Iye atavundukula anaona mwana
wamwamuna akungolira. Iye anamva naye chisoni mwana uja, nati,
"Ameneyu ndi mmodzi mwa ana a Chihebri."

7 Kenaka mlongo wake wa mwanayo anafunsa mwana wa Farao
kuti, "Ndingapite kukakupezerani mmodzi mwa amayi a Chihebri kuti
azikakulererani mwanayu?"

8 Iye anayankha kuti, "Inde, pita." Ndipo mtsikanayo anapita nakayitana
amayi a mwanayo. 9 Mwana wa Farao anati, "Tengani mwanayu
mukandilerere, ndidzakulipirani." Mayiyo anatenga mwanayo kuka-
mulera. 10 Mwanayo atakula anakamupereka kwa mwana wa Farao ndipo
anakhala mwana wake. Iye anamutcha dzina lake Mose, popeza anati,
"Ndinamuvuwula m'madzi."

*Mose Athawira ku Midiyani*

11 Tsiku lina, Mose atakula, anapita kumene kunali anthu a mtundu
wake ndipo anawaona akugwira ntchito yowawa. Iye anaona Mwigupto
akumenya Mhebri, mmodzi mwa anthu a mtundu wake. 12 Atayang'ana
uku ndi uku, naona kuti panalibe wina aliyense, Mose anamupha Mwigup-
toyo ndipo anamukwirira mu mchenga. 13 Mmawa mwake Mose anapita
ndipo anaona anthu awiri a Chihebri akumenyana. Iye anafunsa amene
anali wolakwa kuti, "Chifukwa chiyani ukumenya Mhebri mnzako?"

14 Munthu uja anati, "Kodi ndani anakuyika kuti ukhale wotilamulira
ndi wotiweruza? Kodi ukufuna kundipha monga momwe unaphera
Mwigupto uja?" Mose anachita mantha ndipo anati mu mtima mwake,
"Chimene ndinachita chija chadziwika."

15 Farao atamva zimenezi anafuna kuti aphe Mose, koma Mose anathawa
ndipo anapita kukakhala ku Midiyani. Ali kumeneko, tsiku lina anakhala
pansi pafupi ndi chitsime. 16 Wansembe wa ku Midiyaniko anali ndi ana
aakazi asanu ndi awiri. Iwowa anabwera kudzatunga madzi ndi kudzaza
mu zomwera kuti amwetse nkhosa za abambo awo. 17 Koma kunabwera
abusa ena amene anathamangitsa atsikana aja. Ndiye Mose anayimirira
nawathandiza atsikana aja ndi kumwetsa nkhosa zawo.

18 Atsikana aja atabwerera kwa abambo awo Reueli, iye anawafunsa
kuti, "Chifukwa chiyani lero mwabwera msanga?"

19 Atsikanawo anayankha kuti, "Mwigupto wina ndiye watilanditsa kwa
abusa. Ndiponso anatitungira madzi ndi kumwetsa ziweto zathu."

20 Tsono Reueli anafunsa ana ake kuti, "Ndiye ali kuti munthuyo?
Chifukwa chiyani mwamusiya? Kamuyitaneni kuti adzadye."

21 Mose anavomera kukhala ndi Reueli, ndipo anamupatsa Zipora kuti
akhale mkazi wake. 22 Zipora anabereka mwana wa mwamuna amene
Mose anamutcha Geresomu, popeza anati, "Ndakhala mlendo m'dziko la
eni."
23 Nthawi yonseyo n'kuti ana a Israeli akulira chifukwa cha ukapolo
wawo uja. Iwo anafuwula kupempha thandizo, ndipo kulira kwawoko
kunafika kwa Mulungu. 24 Mulungu anamva kubuwula kwawo ndipo
anakumbukira pangano lake ndi Abrahamu, Isake ndi Yakobo. 25 Mulungu
ataona Aisraeli aja ndi masautso awo, Iye anawamvera chifundo.

# 3

*Kuyitanidwa kwa Mose pa Chitsamba Choyaka Moto*

1 Tsono Mose amaweta ziweto za mpongozi wake Yetero, wansembe uja
wa ku Midiyani. Tsiku lina iye anazitsogolera kupita ku chipululu ndipo
anafika ku phiri la Mulungu lotchedwa Horebu. 2 Kumeneko mngelo wa
Yehova anaonekera kwa iye m'malawi amoto m'chitsamba. Mose anaona
kuti ngakhale chitsambacho chimayaka koma sichimanyeka. 3 Tsono Mose
anati mu mtima mwake, "Ine ndipita komweko ndikaone zodabwitsazi,
chitsamba sichikunyeka chifukwa chiyani?"
4 Yehova ataona kuti Mose anapatuka kuti adzaonetsetse, Mulungu
anamuyitana Mose kuchokera m'chitsambamo nati, "Mose! Mose!"
Ndipo anayankha, "Wawa."
5 Mulungu anati, "Usayandikire kuno. Vula nsapato zako, pakuti malo
amene wayimapo ndi opatulika." 6 Mulungu anati, "Ine ndine Mulungu
wa makolo ako, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake, ndi Mulungu
wa Yakobo." Atamva zimenezi, Mose anaphimba nkhope yake chifukwa
anaopa kuona Mulungu.
7 Yehova anati, "Ine ndaona ndithu mazunzo a anthu anga amene
ali ku Igupto. Ndamva kulira kwawo chifukwa cha anthu amene
akuwapsinja, ndipo ndakhudzidwa ndi masautso awo. 8 Choncho ndab-
wera kuti ndiwapulumutse m'dzanja la Aigupto, kuwatulutsa m'dzikolo
ndi kukawalowetsa m'dziko labwino ndi lalikulu, dziko loyenda mkaka
ndi uchi, kwawo kwa Akanaani, Ahiti, Aamori, Aperezi, Ahivi ndi Ayebusi.
9 Ine ndamva ndithu kulira kwa Aisraeli, ndipo ndaona mmene Aigupto
akuwazunzira. 10 Kotero tsopano, pita. Ine ndikukutuma kwa Farao kuti
ukatulutse anthu anga, Aisraeli m'dziko la Igupto."
11 Koma Mose anafunsa Mulungu, "Ine ndine yani kuti ndipite kwa Farao
ndi kukatulutsa Aisraeli m'dziko la Igupto?"
12 Ndipo Mulungu anati, "Ine ndidzakhala nawe, ndipo ichi chidzakhala
chizindikiro kwa iwe kuti ndine amene ndakutuma; Ukadzatulutsa anthu
anga m'dziko la Igupto, udzapembedza Mulungu pa phiri lino."
13 Mose anati kwa Mulungu, "Ngati ndipita kwa Aisraeli ndi
kukawawuza kuti, 'Mulungu wa makolo anu wandituma kwa inu,' ndipo
iwo n'kukandifunsa kuti 'Dzina lake ndi ndani?' Tsono ine ndikawawuze
chiyani?"
14 Mulungu anati kwa Mose, "NDINE AMENE NDILI. Izi ndi zimene
ukanene kwa Aisraeli: 'NDINE wandituma kwa inu.' "
15 Mulungu anatinso kwa Mose, "Ukanene kwa Aisraeli kuti 'Yehova,
Mulungu wa makolo anu, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake, ndi
Mulungu wa Yakobo, wandituma kwa inu.' Ili ndilo dzina langa mpaka
muyaya, ndipo mibado ya m'tsogolomo izidzanditchula ndi dzina limeneli.

16 “Pita, ukawasonkhanitse akuluakulu a Israeli ndipo ukati kwa
iwo, ‘Yehova, Mulungu wa makolo anu, Mulungu wa Abrahamu, Isake
ndi Yakobo, anandionekera ndipo akuti Iye wadzakuyenderani ndipo
waona mmene Aigupto akukuzunzirani. 17 Choncho wanenetsa kuti
adzakutulutsani m’dziko la Igupto, dziko la masautsoli kupita ku dziko la
Akanaani, Ahiti, Aamori Aperezi, Ahivi ndi Ayebusi, dziko loyenda mkaka
ndi uchi.’
18 “Akuluakulu a Israeli akakumvera. Kenaka iwe ndi akuluakuluwo
mukapite kwa mfumu ya Igupto ndipo mukanene kuti, ‘Yehova, Mulungu
wa Ahebri, wakumana nafe. Tsono tikukupemphani kuti mutilole tipite
pa ulendo wa masiku atatu m’chipululu kuti tikapereke nsembe kwa
Yehova Mulungu wathu.’ 19 Koma Ine ndikudziwa kuti mfumu ya Igupto
sikakulolani kuti mupite pokhapokha Ine nditayikakamiza. 20 Tsono
Ine ndidzatambasula dzanja langa ndi kukantha Aigupto ndi zodabwitsa
zanga zimene ndidzazichita pakati pawo. Zikadzatha izi, Iye adzakulolani
kuti mupite.
21 “Ndipo ine ndidzafewetsa mtima wa Aigupto pa anthu anga,
kotero kuti mukadzatuluka simudzapita wopanda kanthu. 22 Mkazi
aliyense adzapemphe Mwigupto woyandikana naye ndiponso mkazi
amene akukhala m’nyumba yake, kuti amupatse ziwiya za siliva ndi golide
ndiponso zovala zimene mudzaveka ana anu aamuna ndi aakazi. Ndipo
potero mudzawalanda zonse Aiguptowo.”

# 4

*Mulungu Apatsa Mose Mphamvu Zochita Zodabwitsa*

1 Mose anayankha, “Aisraeliwo sakandikhulupirira ndipo
sakandimvera. Iwowo adzati, ‘Yehova sanakuonekere iwe.’ ”
2 Ndipo Yehova anamufunsa nati, “N’chiyani chili m’dzanja lakolo?”
Mose anayankha kuti, “Ndodo.”
3 Yehova anati, “Tayiponya pansi.”
Mose anayiponya pansi ndipo inasanduka njoka ndipo anayithawa.
4 Kenaka Yehova anati kwa iye, “Igwire mtchira.” Ndipo Mose anayigwira
mchira njokayo ndipo inasandukanso ndodo m’dzanja lake. 5 Yehova
anati, “Ukachite zimenezi ndipo akakukhulupirira kuti Yehova, Mulungu
wa makolo awo, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake ndi Mulungu
wa Yakobo, wakuonekera iwe.”
6 Yehova anatinso, “Pisa dzanja lako m’malaya akowo.” Choncho Mose
anapisa dzanja lake m’malaya ake ndipo pamene analitulutsa, linali la
khate kuchita kuti mbuu ngati ufa.
7 Yehova anati, “Tsopano pisanso dzanja lako m’malaya.” Mose
anapisanso dzanja lakelo m’malaya ake ndipo atalitulutsa, linali labwinob-
wino, ngati thupi lake lonse.
8 Tsono Yehova anati “Akakapanda kukukhulupirira, osalabadira choz-
izwitsa choyambacho, akakhulupirira ndithu chifukwa cha chozizwitsa
chachiwiricho. 9 Koma ngati sakakhulupirira zizindikiro ziwiri izi kapena
kukumvera, ukatunge madzi a mu mtsinje wa Nailo ndi kuwathira pa
mtunda powuma ndipo madziwo adzasanduka magazi.”
10 Mose anati kwa Yehova, “Chonde Ambuye, chikhalire ine ndakhala
munthu wosatha kuyankhula bwino. Ngakhale tsopano pamene
mukundiyankhula, lilime langa ndi lolemera. Ndine wachibwibwi.”
11 Yehova anati kwa iye, “Kodi anapatsa munthu pakamwa ndani?
Ndani amasandutsa munthu kuti akhale wosayankhula kapena wosamva?

Ndani amapanga munthu kukhala wopenya kapena wosaona? Kodi si
Ine Yehova? 12 Tsopano pita, Ine ndidzakuthandiza kuyankhula ndipo
ndidzakulangiza zoti ukanene."

13 Koma Mose anati, "Chonde Ambuye, pepani, tumani wina kuti
akachite zimenezi."

14 Kenaka Yehova anamupsera mtima Mose ndipo anati, "Kodi suli
ndi m'bale wako Aaroni wa fuko la Levi? Ine ndikudziwa kuti iye
amayankhula bwino. Iye wanyamuka kale kudzakumana nawe ndipo
adzasangalala akadzakuona. 15 Iwe udzayankhula naye ndi kumuwuza
mawu oti akanene. Ine ndidzakuthandizani kuyankhula nonse awirinu
ndi kukulangizani zoti mukachite. 16 Iye akayankhula kwa anthu m'malo
mwako. Iye adzakhala wokuyankhulira ndipo iweyo udzakhala ngati
Mulungu kwa iye. 17 Koma utenge ndodo imene ili m'dzanja lakoyo kuti
ukachite nayo zizindikiro zozizwitsa."

### *Mose Abwerera ku Igupto*

18 Tsono Mose anabwerera kwa Yetero, mpongozi wake ndipo anati kwa
Iye, "Chonde ndiloleni kuti ndibwerere ku Igupto kwa anthu anga kuti
ndikaone ngati ali moyo."

Yeteri anati, "Pitani mu mtendere."

19 Nthawiyi Yehova anali atamuwuza kale Mose ku Midiyani kuti,
"Bwerera ku Igupto, pakuti anthu onse amene amafuna kukupha aja
anamwalira." 20 Kotero Mose anatenga mkazi wake ndi ana ake aamuna,
ndipo anawakweza pa bulu nayamba ulendo wobwerera ku Igupto. Ndipo
anatenga ndodo ya Mulungu ija m'dzanja lake.

21 Yehova anati kwa Mose, "Ukaonetsetse kuti wachita pamaso pa Farao
zodabwitsa zonse zimene ndayika mphamvu mwa iwe kuti ukachite.
Koma Ine ndidzawumitsa mtima wake kotero kuti sadzalola anthuwo kuti
apite. 22 Ndipo iwe ukati kwa Farao, 'Yehova akuti, Israeli ali ngati mwana
wanga wachisamba.' 23 Choncho ndikuti, 'Mulole mwana wanga apite
kuti akandipembedze. Koma ngati ukana, Ine ndidzapha mwana wako
wachisamba.' "

24 Pambuyo pake Mose ali m'njira, pamalo wogona, Yehova anakumana
naye, ndipo anafuna kumupha. 25 Koma Zipora anatenga mwala
wakuthwa nachita mdulidwe mwana wake ndipo khungulo analikhudz-
itsa pa mapazi a Mose. Iye anati "Zoonadi, kwa ine ndiwe mkwati
wamagazi." 26 Choncho Yehova anamuleka Mose wosamupha. Pa
nthawiyo, Zipora anati, "Mkwati wa magazi," ponena za mdulidwe.

27 Yehova anati kwa Aaroni, "Pita ku chipululu ukakumane ndi Mose."
Iye anapitadi nakakumana ndi Mose pa phiri la Mulungu namupsomp-
sona. 28 Kenaka Mose anamufotokozera Aaroni chilichonse chimene
Yehova anamutuma kuti akanene. Anamufotokozera za zizindikiro
zozizwitsa zimene anamulamulira kuti akazichite.

29 Mose ndi Aaroni anapita kukasonkhanitsa pamodzi akuluakulu onse a
Aisraeli. 30 Ndipo Aaroni anawafotokozera zonse zimene Yehova ananena
kwa Mose. Anachita zizindikirozo pamaso pa anthu onse, 31 ndipo
anakhulupirira. Iwo atamva kuti Yehova anadzawayendera ndi kuti
waona mmene akuzunzikira, anaweramitsa mitu pansi napembedza.

## 5

### *Mose Akumana ndi Farao*

1 Zitachitika izi, Mose ndi Aaroni anapita kwa Farao ndipo anati,
"Yehova Mulungu wa Israeli akuti, 'Aloleni anthu anga apite, kuti akachite
chikondwerero cha Ine m'chipululu.' "

2 Koma Farao anati, "Yehova ndani kuti ine ndimumvere ndi kulola
Aisraeli kuti apite? Ine Yehova sindikumudziwa ndipo sindilola kuti
Aisraeli apite."

3 Ndipo iwo anati, "Mulungu wa Ahebri anakumana nafe. Chonde
tiloleni tipite ulendo wa masiku atatu ku chipululu kuti tikapereke nsembe
kwa Yehova Mulungu wathu, ngati sititero iye adzatipweteka ndi miliri
kapena lupanga."

4 Koma mfumu ya Igupto inati, "Mose ndi Aaroni, chifukwa chiyani
mukuchititsa anthuwa kuti asagwire ntchito zawo? Bwererani ku ntchito
zanu!" 5 Ndiponso Farao anati, "Taonani, anthuwa m'dziko muno alipo
ochuluka, ndipo inu mukuwaletsa kugwira ntchito."

### *Njerwa Zopanda Udzu*

6 Pa tsiku lomwelo Farao analamulira akapitawo a thangata ndi anzawo
a Chiisraeli amene ankayang'anira anthu kuti 7 "Inu musawapatsenso
udzu wopangira njerwa monga mumachitira kale, iwo azipita ndi
kukatenga udzu wawo. 8 Koma musawachepetsere chiwerengero cha
njerwa chomwe munawalamulira kale kuti aziwumba. Iwowa ndi aulesi.
N'chifukwa chake akulira kuti, 'Tiloleni tipite tikapereke nsembe kwa
Mulungu wathu.' 9 Muwakhawulitse ndi ntchito anthu amenewa kuti
azitanganidwa, asakhale ndi mpata omvera zabodza."

10 Choncho akapitawo a thangata ndi anzawo a Chiisraeli amene
ankayang'anira anthu anapita kwa anthu aja nati, " 'Farao akuti sadza-
kupatsaninso udzu. 11 M'malo mwake mupite mukadzimwetere udzu
kulikonse kumene mungawupeze. Komabe ntchito yanu sichepetsedwa.' "
12 Kotero anthuwo anamwazikana m'dziko lonse la Igupto kukamweta
udzu. 13 Akapitawo a thangata aja anawafulumiza anthu aja nati,
"Malizani kugwira ntchito yanu ya tsiku ndi tsiku monga mmene zinalili
pamene munkapatsidwa udzu." 14 Akapitawo a thangata a Farao
ankawamenya oyang'anira anzawo a Chiisraeli aja nawapanikiza kuti,
"Chifukwa chiyani lero simunawumbe chiwerengero chovomerezeka cha
njerwa monga chakale chija?"

15 Pamenepo oyang'anira anzawo a Chiisraeli aja anapita kukadandaula
kwa Farao kuti, "Chifukwa chiyani mwachitira antchito anu zotere?
16 Antchito anu sakupatsidwa udzu, komabe akutiwuza kuti, 'Umbani
njerwa!' Antchito anu akumenyedwa, koma cholakwa sichili ndi anthu
anu."

17 Farao anati, "Ulesi, inu ndinu alesi! N'chifukwa chake mukumanena
kuti, 'Mutilole tipite kukapereka nsembe kwa Yehova.' 18 Pitani tsopano
kuntchito. Simudzapatsidwanso udzu komabe muyenera kuwumba
muyeso wanu wovomerezeka wa njerwa."

19 Oyang'anira anzawo a Chiisraeli anazindikira kuti ali pa mavuto
pamene anawuzidwa kuti, "Musachepetse chiwerengero cha njerwa
chimene muyenera kuwumba tsiku lililonse." 20 Atachoka pamaso pa
Farao, anakumana ndi Mose ndi Aaroni akuwadikira, 21 ndipo iwo anati,
"Yehova akupenyeni ndi kukuweruzani popeza mwachititsa Farao ndi
nduna zake kuti anyansidwe nafe ndipo mwayika lupanga m'manja
mwawo kuti atiphe."

### *Mulungu Alonjeza Chipulumutso*

22 Mose anabwerera kwa Yehova ndipo anati, “Chonde Ambuye, chi-
fukwa chiyani mukuzunza anthu anu? Kodi munanditumira zimenezi?
23 Chipitireni changa kwa Farao kukamuyankhula m’dzina lanu, iye
wakhala akuzunza anthuwa, ndipo inu simunawapulumutse konse anthu
anu.”

# 6

1 Yehova anawuza Mose kuti, “Tsopano udzaona zimene ndimuchite
Farao: Chifukwa cha dzanja langa lamphamvu adzalola anthu anga kuti
atuluke. Chifukwa cha dzanja langa lamphamvu adzawatulutsa m’dziko
lake.”
2 Mulungu anatinso kwa Mose, “Ine ndine Yehova. 3 Ndinaonekera kwa
Abrahamu, kwa Isake ndi kwa Yakobo monga Mulungu Wamphamvu-
zonse, koma sindinawadziwitse dzina langa kuti ndine Yehova.
4 Ndinakhazikitsa pangano langa ndi iwo kuwalonjeza kuti ndidzawapatsa
dziko la Kanaani kumene anakhalako kale ngati alendo. 5 Ndamvanso
kubuwula kwa Aisraeli, amene Aigupto awayesa akapolo ndipo ndakum-
bukira pangano langa.”
6 “N’chifukwa chake nena kwa Aisraeli kuti, ‘Ine ndine Yehova, ndipo
ndidzakutulutsani m’goli la Aigupto. Ndidzakumasulani mu ukapolo,
ndidzakuwombolani ndi dzanja langa lotambasuka ndi kuchita ntchito
zachiweruzo. 7 Ndidzakutengani kukhala anthu anga, ndipo Ine ndidza-
khala Mulungu wanu. Pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova
Mulungu wanu amene ndinakutulutsani m’goli la Aigupto. 8 Ndipo
ndidzakufikitsani ku dziko limene ndinalumbira kuti ndidzalipereka kwa
Abrahamu, kwa Isake ndi kwa Yakobo. Ndidzakupatsani dziko limenelo
kuti likhale lanu. Ine ndine Yehova.’ ”
9 Mose anawafotokozera Aisraeli zimenezi, koma iwo sanamumvere
chifukwa cha kukhumudwa ndi goli lankhanza.
10 Kenaka Yehova anati kwa Mose, 11 “Pita ukawuze Farao mfumu ya
Igupto kuti awalole Aisraeli atuluke m’dziko lake.”
12 Koma Mose ananena kwa Yehova kuti, “Ngati Aisraeli sanandim-
vere, Farao akandimvera chifukwa chiyani, pajatu sinditha kuyankhula
bwino?”

### *Mibado ya Mose ndi Aaroni*

13 Ndipo Yehova analamula Mose ndi Aaroni kuti awuze Aisraeli ndi
Farao mfumu ya Igupto kuti Aisraeli ayenera kutuluka m’dziko la Igupto.

14 Atsogoleri a mafuko awo anali awa:

Ana a Rubeni mwana wachisamba wa Israeli anali Hanoki, Palu,
Hezironi ndi Karimi. Awa anali mafuko a Rubeni.
15 Ana a Simeoni anali Yemueli, Yamini, Ohadi, Yakini, Zohari ndi Saulo
mwana wa kwa mkazi wa Chikanaani. Awa anali mafuko a Simeoni.
16 Mayina a ana a Levi pamodzi ndi zidzukulu zawo anali awa:
Geresoni, Kohati ndi Merari. Levi anakhala ndi moyo kwa zaka 137.
17 Ana a Geresoni, mwa mafuko awo, anali Libini ndi Simei.
18 Ana a Kohati anali Amramu, Izihari, Hebroni ndi Uzieli. Kohati
anakhala ndi moyo zaka 133.
19 Ana a Merari anali Mali ndi Musi.
Awa anali mafuko a Levi monga mwa mibado yawo.

20 Amramu anakwatira Yokobedi mlongo wa abambo ake, amene
anabereka Aaroni ndi Mose. Amramu anakhala ndi moyo kwa zaka
137.

21 Ana a Izihari anali Kora, Nefegi ndi Zikiri.

22 Ana a Uzieli anali Misaeli, Elizafani ndi Sitiri.

23 Aaroni anakwatira Eliseba, mwana wamkazi wa Aminadabu,
mlongo wa Nasoni ndipo Iye anabereka Nadabu, Abihu, Eliezara ndi
Itamara.

24 Ana a Kora anali Asiri, Elikana ndi Abiasafu. Awa ndiwo mafuko a
Kora.

25 Eliezara mwana wa Aaroni anakwatira mmodzi mwa ana aakazi a
Putieli, ndipo anabereka Finehasi.

Awa anali atsogoleri a mabanja a Levi, monga mwa mafuko awo.

26 Aaroni ndi Mose ndi aja amene Yehova anawawuza kuti, “Tulutsani
Aisraeli mu Igupto m’magulu awo.” 27 Mose ndi Aaroni ndiwo amene
anayankhula ndi Farao mfumu ya Igupto kuti atulutse Aisraeli mu Igupto.

### *Aaroni Ayankhula M’malo mwa Mose*

28 Tsopano pamene Yehova anayankhula kwa Mose mu Igupto, 29 anati,
“Ine ndine Yehova. Umuwuze Farao mfumu ya Igupto zonse zimene Ine
ndikuwuze iwe.”

30 Koma Mose anati kwa Yehova, “Farao akandimvera bwanji, pakuti ine
sinditha kuyankhula bwino?”

## 7

1 Ndipo Yehova anati kwa Mose, “Taona ine ndakuyika kuti ukhale
ngati Mulungu kwa Farao, ndipo m’bale wako Aaroni adzakhala mneneri
wako. 2 Iwe ukanene zonse zimene ndakulamulirazi, ndipo Aaroni m’bale
wako ndiye akaziyankhule kwa Farao kuti atulutse ana a Israeli m’dziko
la Igupto. 3 Koma ndidzawumitsa mtima wa Farao, ndipo ngakhale
nditachulukitsa zizindikiro zozizwitsa ndi zodabwitsa mu Igupto, 4 iyeyo
sadzakumverani. Choncho ndidzakantha Igupto, ndipo ndi ntchito
zachiweruzo ndidzatulutsa magulu anga, anthu anga Aisraeli kuwachotsa
m’dziko la Igupto. 5 Ndipo Aigupto adzadziwa kuti Ine ndine Yehova,
ndikadzatambasula dzanja langa kukantha Igupto ndi kutulutsa Aisraeli
m’dzikomo.”

6 Mose ndi Aaroni anachita monga momwe Yehova anawalamulira.
7 Mose anali ndi zaka 80, ndipo Aaroni anali ndi zaka 83 pamene
anakayankhula kwa Farao.

### *Ndodo ya Aaroni Isanduka Njoka*

8 Yehova anati kwa Mose ndi Aaroni, 9 “Ngati Farao adzati kwa inu,
‘Chitani chozizwitsa,’ iwe Mose udzati kwa Aaroni, ‘Tenga ndodo yako
ndipo uyiponye pamaso pa Farao,’ ndipo idzasanduka njoka.”

10 Kotero Mose ndi Aaroni anapita kwa Farao ndi kuchita monga momwe
Yehova anawalamulira. Aaroni anaponya ndodo yake pansi patsogolo pa
Farao ndi nduna zake ndipo inasanduka njoka. 11 Naye Farao anayitanitsa
anthu ake anzeru ndi amatsenga, ndipo nawonso amatsenga a Chiigupto
anachita zinthu zomwezo mwa matsenga awo. 12 Aliyense wa iwo
anaponya ndodo yake pansi ndipo inasanduka njoka. Koma ndodo ya

Aaroni inameza ndodo zawo. 13 Koma mtima wa Farao unawuma ndipo
sanawamvere monga momwe Yehova ananenera.

### *Mliri wa Magazi*

14 Kenaka Yehova anati kwa Mose, "Farao ndi wowuma mtima. Akukana
kulola anthu anga kuti apite. 15 Upite kwa Farao mmawa pamene
azidzapita ku madzi. Ukamudikire m'mbali mwa Nailo kuti ukakumane
naye ndipo unyamule ndodo imene inasanduka njoka ija m'dzanja lako.
16 Ndipo ukamuwuze Farao kuti, 'Yehova, Mulungu wa Ahebri wandituma
kuti ndikuwuzeni kuti: Lolani anthu anga apite kuti akandipembedze
m'chipululu. Koma mpaka tsopano inu simunandimvere. 17 Izi ndi zimene
Yehova akunena: Ndi ndodo imene ili m'dzanja langa ndidzamenya
madzi a mu Nailo, ndipo madzi adzasanduka magazi. Ndikadzachita ichi
udzadziwa kuti Ine ndine Yehova: 18 Nsomba za mu Nailo zidzafa, mtsinje
udzanunkha ndipo Aigupto sadzatha kumwa madzi ake.' "
19 Yehova anati kwa Mose, "Uza Aaroni kuti, 'Tenga ndodo yako
uyilozetse ku madzi a mu Igupto pa mitsinje, pa ngalande, pa zithaphwi
ndi pa madambo, ndipo onse adzasanduka magazi.' M'dziko lonse la
Igupto mudzakhala magazi, ngakhale m'zotungira madzi zopangidwa ndi
mitengo ndi miyala."
20 Mose ndi Aaroni anachita monga momwe Yehova analamulira.
Anakweza ndodo yake pamaso pa Farao ndi akuluakulu ake ndipo
anamenya madzi a mu Nailo, ndipo madzi onse anasanduka magazi.
21 Nsomba za mu Nailo zinafa ndipo mtsinje unanunkha kwambiri kotero
kuti Aigupto sanathe kumwa madzi ake. Magazi anali ponseponse mu
Igupto.
22 Koma amatsenga a Chiigupto anachita zinthu zomwezo mwa mat-
senga awo. Choncho Farao anawumabe mtima, ndipo sanamvere zonena
za Mose ndi Aaroni monga momwe Yehova ananeneratu. 23 M'malo
mwake iye anatembenuka ndi kupita ku nyumba yake yaufumu ndipo
zimenezi sanazilabadire. 24 Anthu onse a ku Igupto anayamba kukumba
m'mbali mwa mtsinje wa Nailo kuti apeze madzi akumwa, chifukwa
sanathe kumwa madzi a mu mtsinjemo.

### *Mliri wa Achule*

25 Panapita masiku asanu ndi awiri Yehova atamenya madzi a mu
mtsinje wa Nailo.

## 8

1 Kenaka Yehova anati kwa Mose, "Ukamuwuze Farao kuti, Lolani anthu
anga kuti apite, akandipembedze. 2 Ndipo ngati simulola kuti apite Ine
ndidzalanga dziko lonse la Igupto polidzaza ndi achule. 3 Mtsinje wa Nailo
udzadzaza ndi achule. Achulewo adzatuluka ndi kukalowa m'nyumba
yaufumu, ku chipinda chogona ndi pa bedi lako, m'nyumba za nduna
zako ndi pa anthu ako ndi mophikira buledi ndiponso mopangira bulediyo.
4 Achulewo adzakulumphira iwe ndi anthu ako ndiponso nduna zako."
5 Ndipo Yehova anati kwa Mose, "Uza Aaroni kuti, 'Loza ndodo yako
ku mitsinje, ku ngalande ndi ku zithaphwi ndipo pakhale achule pa dziko
lonse la Igupto.' "
6 Kotero Aaroni analoza dzanja lake pa madzi a ku Igupto, ndipo achule
anatuluka nadzaza dziko lonse la Igupto. 7 Koma amatsenga anachita
zinthu zomwezo m'matsenga awo. Iwonso anatulutsa achule m'dziko
lonse la Igupto.

8 Kenaka, Farao anayitanitsa Mose ndi Aaroni ndipo anati, “Pemphera
kwa Yehova kuti achulewa achoke kwa ine ndi anthu anga, ndipo ine
ndidzalola kuti anthu anu apite kukapereka nsembe kwa Yehova.”
9 Mose anati kwa Farao, “Inu mungonditchulira nthawi imene mukufuna
kuti ndikupempherereni, nduna zanu pamodzi ndi anthu anu kuti achule
achoke m’nyumba zanu ndi kuti atsale okhawo ali mu mtsinje wa Nailo.”
10 Farao anati, “Mawa.”
Mose anamuyankha kuti, “Chabwino zidzakhala monga mwaneneramu,
kuti mudzadziwe kuti palibe wina wofanana ndi Yehova Mulungu wathu.
11 Achule adzachoka m’nyumba yanu, m’nyumba za nduna zanu pamodzi
ndi za anthu anu. Koma adzatsala mu mtsinje wa Nailo basi.”
12 Mose ndi Aaroni anachoka, ndipo Mose anapemphera kwa Yehova
kuti achotse achule amene anatumiza kwa Farao. 13 Ndipo Yehova
anachita zomwe Mose anapempha. Achule amene anali m’nyumba,
m’mabwalo ndi m’minda anafa 14 Aigupto anawunjika achulewo milumilu
ndipo dziko linanunkha. 15 Koma Farao ataona kuti zinthu zinayambanso
kukhala bwino, anawumitsanso mtima wake ndipo sanamverenso mawu
a Mose ndi Aaroni, monga momwe Yehova ananenera.

### *Mliri wa Nsabwe*

16 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Uza Aaroni kuti akweze ndodo yake
ndi kumenya fumbi la pa nthaka, ndipo fumbilo lidzasanduka nsabwe pa
dziko lonse la Igupto.” 17 Iwo anachita momwemo, ndipo pamene Aaroni
anakweza ndodo yake ndi kumenya fumbi, nsabwe zinafika pa munthu
aliyense ndi pa ziweto. Fumbi lonse la m’dziko la Igupto linasanduka
nsabwe. 18 Koma amatsenga atayesa kupanga nsabwe mwa matsenga awo,
analephera. Ndipo nsabwezo zinali pa munthu aliyense ndi pa ziweto
zawo.
19 Amatsenga anati kwa Farao, “Izi wachita ndi Mulungu.” Koma mtima
wa Farao unali wowumabe ndipo sanamvere zonena za Mose ndi Aaroni
monga momwe Yehova ananenera.

### *Mliri wa Ntchentche Zoluma*

20 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Mmawa, upite ukakumane ndi Farao
maso ndi maso pamene azidzapita ku madzi ndipo ukanene kuti, ‘Yehova
akuti, Lola anthu anga kuti apite akandipembedze. 21 Koma ngati suwalola
anthu anga kuti apite, Ine ndidzatumiza pa iwe ntchentche zoluma ndi pa
nduna zako ndi anthu ako ndi m’nyumba zanu. M’nyumba za Aigupto
mudzadzaza ntchentche zoluma. Ngakhale pa nthaka pamene akhalapo
padzadzaza ndi ntchentche zoluma.’ ”
22 “Koma pa tsikulo ndidzapatula dera la Goseni, kumene kumakhala
anthu anga, motero kuti sikudzakhala ntchentche zoluma. Choncho
iwe udzadziwa kuti Ine Yehova ndi amene ndikulamulira dziko lino.
23 Ndidzasiyanitsa pakati pa anthu anga ndi anthu ako. Chizindikiro
chozizwitsa ichi chidzachitika mawa.”
24 Ndipo Yehova anachita zimenezi: Ntchentche zoluma zochuluka
zinalowa m’nyumba yaufumu ya Farao ndi nyumba za nduna zake.
Choncho ntchentche zolumazi zinawononga dziko lonse la Igupto.
25 Kenaka Farao anayitanitsa Mose ndi Aaroni nati, “Pitani kaperekeni
nsembe kwa Mulungu wanu m’dziko lomwe lino.”
26 Koma Mose anati, “Sitingathe kutero pakuti nsembe zathu kwa Yehova
Mulungu ndi zowayipira Aigupto. Ngati tipereke nsembe zowayipira
Aigupto m’maso mwawo, adzatiponya miyala kuti tife. 27 Ife tiyenera

kuyenda ulendo wa masiku atatu kupita ku chipululu kukapereka nsembe
kwa Yehova Mulungu wathu monga anatilamulira.”
28 Farao anati, “Ine ndikulolani kuti mupite ku chipululu kukapereka
nsembe kwa Yehova Mulungu wanu, koma musapite kutali kwambiri.
Tsopano ndipemphererenі.”
29 Mose anayankha kuti, “Ine ndikangochoka pano, ndikapemphera
kwa Yehova ndipo mawa lomweli ntchentche zoluma zidzachoka kwa
Farao, nduna zake pamodzi ndi anthu ake. Koma Farao, onetsetsani
kuti musachitenso zachinyengo ndi kuwakaniza anthu kuti asakapereke
nsembe kwa Yehova.”
30 Choncho Mose anasiyana ndi Farao nakapemphera kwa Yehova.
31 Ndipo Yehova anachita zomwe Mose anapempha: Ntchentche zoluma
zinachoka kwa Farao ndi nduna zake ndiponso kwa anthu ake. Palibe
ngakhale imodzi yomwe inatsala. 32 Koma nthawi imeneyinso Farao
anawumitsa mtima wake ndipo sanalole kuti anthu atuluke.

# 9

*Mliri pa Ziweto*

1 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Pita kwa Farao ndipo ukamuwuze
kuti Yehova, Mulungu wa Ahebri akuti alole anthu anga apite kuti
akandipembedze. 2 Koma ngati ukana kuti apite ndi kupitiriza kuwaletsa,
3 dzanja la Yehova lidzakantha ziweto zako zimene zili ku munda, pamodzi
ndi akavalo, abulu, ngamira, ng’ombe, nkhosa ndi mbuzi ndi mliri woopsa
kwambiri. 4 Koma Yehova adzasiyanitsa pakati pa ziweto za Israeli ndi
ziweto za Igupto, kotero kuti palibe chiweto n’chimodzi chomwe cha
Aisraeli chimene chidzafe.”
5 Yehova anayika nthawi ndipo anati, “Yehova adzachita zimenezi
mmawa m’dziko muno.” 6 Ndipo mmawa mwake Yehova anachitadi
zimenezi. Ziweto zonse za Aigupto zinafa, koma palibe chiweto ndi
chimodzi chomwe cha Aisraeli chomwe chinafa. 7 Farao anatuma anthu
kuti akafufuze ndipo anapeza kuti palibe chiweto chilichonse cha Aisraeli
chomwe chinafa. Komabe mtima wake sunagonje ndipo iye sanalole kuti
anthu apite.

*Mliri wa Zotupa*

8 Kenaka Yehova anati kwa Mose ndi Aaroni, “Tapani phulusa la
pa moto lodzaza dzanja ndipo Mose aliwaze mmwamba pamaso pa
Farao. 9 Phulusalo lidzasanduka fumbi pa dziko lonse la Igupto. Tsono
fumbilo lidzasanduka zithupsa zomaphulika n’kukhala zilonda pa munthu
aliyense ndi pa nyama zomwe m’dziko lonse la Igupto.”
10 Kotero anatenga phulusa la pa moto ndi kuyima pamaso pa Farao.
Mose analiwaza mmwamba, ndipo panabuka zotupa zophulika zokha pa
munthu aliyense ndi pa ziweto. 11 Amatsenga sanathe kumuyandikira
Mose chifukwa nawonso anali ndi zithupsa monga mmene analili Aigupto
ena onse. 12 Koma Yehova anawumitsa mtima wa Farao ndipo iye
sanamvere Mose ndi Aaroni monga momwe Yehova anamuwuzira Mose.

*Mliri wa Mvula ya Matalala*

13 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Mawa mmawa upite ukakumane ndi
Farao maso ndi maso ndipo ukamuwuze kuti Yehova Mulungu wa Ahebri
akuti ulole anthu anga apite kuti akandipembedze. 14 Ngati suwalola,
tsopano ndidzagwetsa miliri yanga yonse pa iwe ndi nduna zako ndiponso

pa anthu ako, kuti udziwe kuti palibe wina wofanana nane pa dziko
lonse lapansi. 15 Pakuti ndikanakhala nditatukula kale dzanja langa
ndikupheratu iwe pamodzi ndi anthu ako onse pa dziko lapansi. 16 Koma
ndakuyika kukhala mfumu ndi cholinga choti ndionetse mphamvu zanga
kwa iwe ndiponso kuti dzina langa litchuke pa dziko lonse lapansi.
17 Komabe iwe ukudzitukumula pa anthu anga osawalola kuti atuluke.
18 N'chifukwa chake mawa, nthawi ngati ino, ndidzagwetsa matalala
amphamvu amene sanagwepo pa Igupto, kuyambira pachiyambi mpaka
lero. 19 Tsopano lamula kuti ziweto zanu zonse ndi zinthu zonse zomwe
zili ku minda kuti zilowetsedwe m'khola, chifukwa matalala adzagwera
munthu aliyense ndi chiweto chilichonse chimene sichidzalowetsedwa
m'khola ndipo zimene zidzakhala zili ku munda zidzafa."

20 Nduna za Farao zinachita mantha ndi mawu a Yehova, ndipo
zinalowetsa antchito awo ndi ziweto zawo m'nyumba. 21 Koma iwo amene
ananyozera mawu a Yehova anasiya akapolo ndi ziweto zawo panja.

22 Kenaka Yehova anati kwa Mose, "Kweza dzanja lako kumwamba kuti
matalala agwe pa dziko lonse la Igupto, pa munthu aliyense, pa ziweto
ndi pa zonse zomera m'minda ya Igupto." 23 Mose ataloza ndodo yake
kumwamba, Yehova anatumiza mabingu ndi matalala ndi ziphaliwali
zong'anima pa nthaka. Kotero Yehova anagwetsa matalala pa dziko la
Igupto. 24 Matalala anagwa ndipo ziphaliwali zinang'anima. Inali mphepo
ya mkuntho yoopsa kwambiri imene sinakhaleponso m'dziko lonse la
Igupto chiyambire pamene Aigupto anakhala mtundu woyima pa okha.
25 Matalala anawononga dziko lonse la Igupto, munthu aliyense pamodzi
ndi ziweto. Matalala aja anawononga zomera zonse za m'munda ndi
kukhadzula mtengo uliwonse. 26 Ku malo kokhako kumene matalala
sanafikeko ndi dera la Goseni kumene kunali Aisraeli.

27 Kenaka Farao anayitanitsa Mose ndi Aaroni nati kwa iwo, "Tsopano
ndachimwa, Yehova ndi wolungama, ine ndi anthu anga ndife olakwa.
28 Upemphere kwa Mulungu chifukwa mabingu ndi matalala atikwana.
Ine ndidzakulolani kuti mupite. Simuyenera kukhalabe kuno."

29 Mose anayankha, "Ndikangotuluka mu mzinda muno, ine ndidzak-
weza manja anga kwa Yehova ndi kupemphera. Mabingu ndi matalalawa
adzaleka ndipo inu mudzadziwa kuti Yehova ndiye akulamulira dziko
lapansi. 30 Koma ine ndikudziwa kuti inu ndi nduna zanu simukuopabe
Yehova Mulungu."

31 Thonje ndi barele zinawonongeka, popeza barele anali atakhwima ndi
thonje linali ndi maluwa. 32 Koma tirigu ndi mchewere sizinawonongeke
chifukwa zimakhwima mochedwa.

33 Mose anasiyana ndi Farao natuluka mu mzindawo. Iye anakweza
manja ake kwa Yehova. Mabingu ndi matalala zinaleka, ndipo mvula
inalekeratu kugwa m'dzikolo. 34 Farao ataona kuti mvula, matalala ndi
mabingu zaleka, anachimwanso. Iye ndi nduna zake anawumitsanso
mitima yawo. 35 Choncho Farao sanalole kuti Aisraeli apite monga momwe
Yehova anamuwuzira Mose.

# 10

*Mliri wa Dzombe*

1 Kenaka Yehova anati kwa Mose, "Pita kwa Farao, pakuti Ine ndawu-
mitsa mtima wake ndi mitima ya nduna zake kuti ndichite zizindikiro
zozizwitsa pakati pawo 2 kuti inu mudzawuze ana ndi zidzukulu zanu za

mmene ndinawakhawulitsira Aigupto ndi zizindikiro zozizwitsa zimene
ndinachita pakati pawo ndiponso kuti inu mudziwe kuti ine ndine
Yehova.”
3 Ndipo Mose ndi Aaroni anapita kwa Farao ndi kukanena kuti, “Yehova
Mulungu wa Ahebri, akuti: ‘Kodi udzakanabe kudzichepetsa pamaso
panga mpaka liti? Alole anthu anga apite kuti akandipembedze. 4 Ngati
ukana kuwalola, ndigwetsa dzombe m’dziko lako lino mawa. 5 Dzombeli
lidzakuta nthaka yonse moti sidzaoneka konse. Lidzadya kalikonse
kakang’ono kamene sikanawonongedwe ndi matalala aja, kuphatikizapo
mitengo yonse imene ikumera m’minda yanu. 6 Dzombeli lidzadzaza
nyumba zako ndi za nduna zako ndiponso za Aigupto onse, chinthu
chimene ngakhale makolo anu kapena makolo awo sanachionepo kuyam-
bira tsiku limene anakhala m’dzikoli mpaka lero.’ ” Ndipo Mose ndi Aaroni
anatembenuka ndi kumusiya Farao.
7 Nduna za Farao zinamufunsa kuti, “Kodi munthu uyu adzativutitsa
mpaka liti? Aloleni anthuwa apite, kuti akapembedze Yehova Mulungu
wawo. Kodi simukuona kuti dziko la Igupto lawonongeka?”
8 Choncho Mose ndi Aaroni anayitanidwanso kwa Farao ndipo anati,
“Pitani kapembedzeni Yehova Mulungu wanu. Koma ndani amene
adzapite?”
9 Mose anayankha kuti, “Ife tidzapita tonse pamodzi; ang’onoang’ono
ndi akuluakulu, ana athu aamuna ndi aakazi, ndiponso ziweto zathu ndi
ng’ombe chifukwa tikakhala ndi chikondwerero cha kwa Yehova.”
10 Farao anati, “Yehova akhale ndi inu ngati ndingakuloleni kupita
pamodzi ndi akazi ndi ana anu! Zikuoneka kuti mwakonzeka kuchita
choyipa. 11 Ndakana! Amuna okha ndiwo apite ndi kukapembedza Yehova
pakuti izi ndi zimene mwakhala mukupempha.” Kenaka Mose ndi Aaroni
anathamangitsidwa pamaso pa Farao.
12 Ndipo Yehova anati kwa Mose, “Tambalitsa dzanja lako pa dziko la
Igupto kuti dzombe lidze pa dziko la Igupto ndi kuwononga chilichonse
chimene chikumera m’minda ndi chilichonse chimene chinatsala pa
nthawi ya matalala.”
13 Kotero Mose anakweza ndodo yake pa dziko la Igupto, ndipo Yehova
anawutsa mphepo ya kummawa imene inawomba pa dziko usana ndi
usiku wonse. Mmene kumacha n’kuti mphepoyo itabweretsa dzombe.
14 Dzombelo linafika pa dziko lonse la Igupto ndi kukhala dera lililonse
la dzikolo. Dzombe lambiri ngati limenelo silinakhaleponso n’kale lonse
ndipo silidzakhalapo ngakhale m’tsogolo. 15 Dzombelo linaphimba nthaka
yonse mpaka kuoneka kuti bii. Linadya zonse zimene zinatsala nthawi
ya matalala, zomera za m’munda ndi zipatso. Panalibe chobiriwira
chilichonse chimene chinatsala pa mtengo kapena pa chomera chilichonse
m’dziko lonse la Igupto.
16 Mwamsangamsanga, Farao anayitanitsa Mose ndi Aaroni ndipo anati,
“Ine ndachimwira Yehova Mulungu wanu ndiponso inu. 17 Tsopano
ndikhululukirenso tchimo langa kano konkha ndipo pempherani kwa
Yehova Mulungu wanu kuti andichotsere mliri wosakazawu.”
18 Mose anachoka kwa Farao nakapemphera kwa Yehova. 19 Ndipo
Yehova anasintha mphepo ija kuti ikhale ya mphamvu yochokera ku
madzulo, ndipo inanyamula dzombe lija n’kulikankhira m’Nyanja Yofiira.
Panalibe dzombe ndi limodzi lomwe limene linatsala mu Igupto. 20 Koma
Yehova anawumitsa mtima wa Farao, ndipo sanalole kuti Aisraeli apite.

### *Mliri wa Mdima*

21 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Tambasulira dzanja lako kumwamba
kuti kukhale mdima umene udzaphimba dziko lonse la Igupto, mdima
wandiweyani.” 22 Choncho Mose anakweza dzanja lake kumwamba ndipo
mdima wandiweyani unaphimba dziko lonse la Igupto kwa masiku atatu.
23 Palibe amene anatha kuona mnzake kapena kuchoka pa khomo pake
kwa masiku atatu. Koma kumalo kumene kumakhala Aisraeli kunali
kowala.

24 Kenaka Farao anayitanitsa Mose ndi Aaroni nati, “Pitani kapem-
bedzeni Yehova. Ngakhale akazi ndi ana anu apite pamodzi ndi inu. Koma
musatenge ziweto zanu ndi ng’ombe zanu.”

25 Koma Mose anati, “Ndiye inu mutipatse nsembe zopsereza zoti
tikapereke kwa Yehova Mulungu wathu. 26 Koma ayi, ife tipita ndi
ziweto zathu. Palibe chiweto chilichonse chimene chitatsale kuno,
popeza tikasankha komweko ziweto zokapembedzera Yehova. Sitin-
gadziwe zimene tikagwiritse ntchito popembedza Yehova mpaka titakafika
kumeneko.”

27 Koma Yehova anawumitsa mtima wa Farao ndipo sanafune kuwalola
kuti apite. 28 Farao anati kwa Mose, “Choka pamaso panga! Uwonetsetse
kuti usadzaonekerenso pamaso panga! Tsiku limene ndidzakuonenso
udzafa.”

29 Mose anayankha kuti, “Monga momwe mwaneneramu, Ine sindidza-
onekeranso pamaso panu.”

# 11

### *Mliri wa Imfa ya Ana Oyamba Kubadwa*

1 Tsopano Yehova anati kwa Mose, “Ine ndidzalanga Farao pamodzi ndi
Aigupto onse ndi mliri umodzi wotsiriza. Zikadzachitika izi iye adza-
kulolani kuti mutuluke m’dziko lino. Ndithu pamene azidzakutulutsani
adzachita ngati akukuyingitsani. 2 Awuze anthu kuti mwamuna aliyense
ndi mkazi aliyense apemphe kwa mnansi wake ziwiya zasiliva ndi golide.”
3 Tsono Yehova anachititsa Aigupto kuti akomere mtima Aisraeli. Komanso
Mose anali wotchuka kwambiri m’dziko la Igupto, pamaso pa nduna za
Farao ndi anthu onse.

4 Tsono Mose anawuza Farao kuti, “Pakati pa usiku, Yehova adza-
yenda pakati pa anthu a ku Igupto. 5 Ndipo mwana aliyense wamwa-
muna wachisamba adzafa, kuyambira mwana wamwamuna wa Farao
amene amakhala pa mpando waufumu, mpaka mwana wamwamuna
wachisamba wa mdzakazi wake amene ali naye pa mtondo, komanso
ana oyamba a ziweto. 6 Kudzakhala kulira kwakukulu m’dziko lonse la
Igupto, kumene sikunachitikepo ndipo sikudzachitikanso. 7 Koma pakati
pa Aisraeli, ngakhale galu sadzawuwa munthu aliyense kapena chiweto!”
Kotero mudzadziwa kuti Yehova ndiye wasiyanitsa pakati pa Igupto ndi
Israeli. 8 Nduna zanu zonse zidzabwera kwa ine, kugwada pamaso panga
ndi kunena kuti, “Pita iwe ndi anthu ako onse amene akukutsatirawa!
Zimenezi zikadzachitika ine ndidzachoka.” Ndipo Mose anachoka kwa
Farao atakwiya kwambiri.

9 Yehova ananena kwa Mose kuti, “Farao adzakana kukumvera, kuti
zodabwitsa zanga zichuluke m’dziko la Igupto.” 10 Mose ndi Aaroni
anachita zodabwitsa zonsezi pamaso pa Farao koma Yehova anawumitsa
mtima wa Farao, ndipo sanalole kuti Aisraeli atuluke m’dziko lake.

# 12

### *Kukhazikitsidwa kwa Paska*

1 Yehova anayankhula kwa Mose ndi Aaroni m'dziko la Igupto kuti,
2 "Mwezi uno uzikhala mwezi wanu woyamba wa chaka. 3 Muliwuze
khamu lonse la Israeli kuti pa tsiku la khumi la mwezi uno, munthu
aliyense asankhire banja lake mwana wankhosa mmodzi. Banja lililonse
litenge mwana wankhosa mmodzi. 4 Ngati banja lili lochepa moti
silingathe kudya nyama yonse ya nkhosa, ligawane ndi banja lomwe
layandikana nalo nyumba. Mabanja adziwiretu chiwerengero cha anthu
amene alipo pokonzekera zimenezi. Muwerengere kuchuluka kwa nyama
imene anthu adzadye potengera mmene munthu mmodzi angadyere.
5 Ziweto zimene musankhe ziyenera kukhala zazimuna za chaka chimodzi,
zopanda chilema, ndipo zikhale nkhosa kapena mbuzi. 6 Muzisunge
mpaka tsiku la khumi ndi chinayi la mwezi, pamene gulu lonse la Aisraeli
lidzaphe nyamazo madzulo. 7 Ndipo adzatengeko magazi anyamazo ndi
kuwaza pa mphuthu ziwiri za chitseko ndiponso pamwamba pa chitseko
cha nyumba mmene adzadyeremo ana ankhosawo. 8 Adzawotche nya-
mayo ndi kudya usiku womwewo, ndipo adzayidye ndi buledi wophikidwa
popanda yisiti pamodzi ndi masamba wowawa. 9 Musadzadye yayi-
wisi kapena yophika, koma mudzawotche yonse, mutu, miyendo ndi
zam'mimba. 10 Musadzasiye nyama ina mpaka mmawa, ngati ina idzatsala
mpaka mmawa, mudzayitenthe. 11 Muzidzadya nyamayo mutavala
chotere, pokonzekera ulendo: mudzazimangirire lamba m'chiwuno,
nsapato zanu kuphazi ndi ndodo yanu kumanja. Mudzadye mofulumira.
Imeneyi ndi Paska ya Yehova.

12 "Usiku umenewo Ine ndidzadutsa m'dziko la Igupto ndipo ndidzapha
chilichonse choyamba kubadwa kuyambira mwana wa munthu aliyense
mpaka ana aziweto. Ndidzalanganso milungu yonse ya Igupto. Ine
ndine Yehova. 13 Magazi amene mudzawaze pa mphuthu za zitseko ndi
pamwamba pa zitseko aja adzakhala ngati chizindikiro. Ine ndikadzaona
magaziwo ndidzakudutsani, ndipo ndikadzamakantha anthu a Igupto,
mliri wosakazawu sudzakukhudzani.

14 "Ili ndi tsiku la chikumbutso. Tsiku limeneli muzidzachita chikondw-
erero, kupembedza Yehova. Mibado yonse imene ikubwera izidza-
kumbukira tsiku limeneli ngati lamulo lamuyaya ndi kuti pa tsikuli
azidzachita chikondwerero cholemekeza Yehova. 15 Kwa masiku asanu
ndi awiri muzidya buledi wopanda yisiti. Tsiku loyamba muzichotsa
yisiti m'nyumba zanu, ngati aliyense adzadya kanthu kalikonse kali
ndi yisiti kuyambira tsiku loyamba mpaka tsiku lachisanu ndi chiwiri,
munthu ameneyo adzayenera kuchotsedwa m'gulu la Israeli. 16 Pa tsiku
loyamba muzichita msonkhano wopatulika, ndipo winanso uzikhala pa
tsiku lachisanu ndi chiwiri. Musamagwire ntchito masiku onsewa, koma
ntchito yokonza chakudya yokha kuti aliyense adye. Izi ndi zimene
muzichita.

17 "Muzichita chikondwerero cha buledi wopanda yisiti, chifukwa ndi pa
tsiku limeneli ndinatulutsa magulu anu m'dziko la Igupto. Muzikondw-
erera tsiku limeneli pa mibado yonse ngati lamulo lamuyaya. 18 Mwezi
woyamba muzidzadya buledi wopanda yisiti kuyambira madzulo tsiku la
14 la mweziwo mpaka tsiku la 21 mwezi womwewo. 19 Yisiti asamapezeka
m'nyumba zanu kwa masiku asanu ndi awiri. Ndipo aliyense amene adya
chakudya chimene muli yisiti, munthu ameneyo ayenera kuchotsedwa
m'gulu la Aisraeli, kaya iyeyo ndi mlendo kapena mbadwa. 20 Musadye

chilichonse chokhala ndi yisiti. Kulikonse kumene mukukhala, muyenera kudya buledi wopanda yisiti."

21 Ndipo Mose anasonkhanitsa akuluakulu onse a Israeli nati, "Pitani msanga kukasankha nkhosa zokwanira pa mabanja anu, ndipo
muziphe ngati Paska. 22 Mutengenso nthambi ya chitsamba cha hisope,
muchiviyike m'magazi amene mwawayika m'beseni ndipo muwaze ena mwa magaziwo pamwamba ndi m'mbali mwa mphuthu za chitseko. Palibe aliyense wa inu amene adzatuluke m'nyumba yake mpaka mmawa.
23 Pamene Yehova adzadutsa m'dziko kudzakantha Aigupto, n'kuona magazi pamwamba ndi m'mbali mwa mphuthu za chitseko, Iye adzadutsa khomo limenelo ndipo sadzalola woononga yo kuti alowe m'nyumba zanu kuti akukantheni.

24 "Muzimvera malamulo amenewa kwa muyaya, inu ndi zidzukulu
zanu. 25 Mukakalowa m'dziko limene Yehova adzakupatseni monga
analonjeza, mukasunge mwambo umenewu. 26 Ndipo ana anu akakakufunsani kuti, 'Mwambo umenewu ukutanthauza chiyani?' 27 Inu
mukawawuze kuti, 'Ndi nsembe ya Paska ya Yehova, popeza pamene ankakantha nyumba za Aigupto anasiya nyumba zathu.' " Kenaka anthu
anawerama napembedza. 28 Aisraeli anachita monga momwe Yehova analamulira Mose ndi Aaroni.

29 Pakati pa usiku Yehova anakantha ana onse oyamba kubadwa m'dziko la Igupto, kuyambira woyamba kubadwa wa Farao, amene amakhala pa mpando waufumu wa Faraoyo, mpaka mwana woyamba kubadwa wa munthu amene anali m'dzenje, pamodzinso ndi ana oyamba kubadwa
a ziweto zawo. 30 Farao ndi nduna zake zonse ndiponso Aigupto onse anadzuka pakati pa usiku, ndipo kunali kulira kwakukulu m'dziko lonse la Igupto, pakuti panalibe nyumba imene munalibe munthu wakufa.

### *Kutuluka kwa Aisraeli*

31 Pakati pa usiku Farao anayitanitsa Mose ndi Aaroni ndipo anati, "Nyamukani! Asiyeni anthu anga, inu ndi Aisraeli! Pitani, kapembedzeni
Yehova monga munapempha. 32 Tengani ziweto ndi ng'ombe zanu ndipo pitani kapembedzeni Mulungu wanu monga munanenera kuti ine ndidalitsike."

33 Aigupto anawawumiriza anthuwo kuti atuluke mofulumira ndi kusiya
dziko lawo. Iwo anati, "Ngati sitiwalola kutero, tonse tidzafa." 34 Motero
anthuwo ananyamula ufa wawo wopangira buledi asanathiremo yisiti ndipo anasenza pa mapewa awo pamodzi ndi zokandiramo buledi atazikulunga mu nsalu. 35 Aisraeli anachita monga anawawuzira Mose kuti apemphe kwa Aigupto zozikongoletsera zasiliva ndi zagolide ndi zovala.
36 Yehova anafewetsa mtima Aigupto kuti akomere mtima Aisraeliwo ndipo anawapatsa zimene anawapempha. Motero Aisraeli anawalanda zinthu Aigupto.

37 Aisraeli anayenda ulendo kuchokera ku Ramesesi mpaka kukafika ku Sukoti. Anthu aamuna oyenda pansi analipo 600,000 osawerengera
akazi ndi ana. 38 Anthu enanso ambiri anapita nawo, kuphatikizanso
gulu lalikulu la ziweto, mbuzi, nkhosa pamodzi ndi ng'ombe. 39 Iwo
anapanga buledi wopanda yisiti ndi ufa umene anachoka nawo ku Igupto. Ufawo unalibe yisiti chifukwa anachita kuthamangitsidwa ku Igupto ndipo analibe nthawi yokonzera chakudya chawo.

40 Ndipo Aisraeli anakhala ku Igupto kwa zaka 430. 41 Pa tsiku lomwelo
limene anakwanitsa zaka 430, magulu onse a Yehova anatuluka m'dziko la

Igupto. 42 Usiku wonse Yehova anachezera kutulutsa ana a Israeli m'dziko
la Igupto. N'chifukwa chake pa tsiku limeneli Aisraeli onse azichezera
usiku wonse kulemekeza Mulungu kamba ka mibado yonse ya m'tsogolo.

*Lamulo la Paska*

43 Yehova anati kwa Mose ndi Aaroni, "Malamulo a Paska ndi awa:
"Mlendo asadye Paska. 44 Kapolo aliyense amene munagula angadye
ngati atayamba wachita mdulidwe. 45 Koma amene mukukhala naye kwa
kanthawi kapena waganyu asadye Paska.

46 "Muzidyera Paska m'nyumba imodzi. Musatulutse nyama iliyonse
kunja kwa nyumba. Musaswe mafupa aliwonse. 47 Gulu lonse la Israeli
lizichita mwambo wachikondwererochi.

48 "Ngati mlendo wokhala pakati panu angafune kuchita nawo
mwambo wa chikondwerero cha Paska, cha Yehovachi, amuna onse a
m'nyumba mwake ayenera kuchita mdulidwe. Akatero muzimutenga
ngati mbadwa pakati panu. Koma aliyense wosachita mdulidwe asadye
Paska. 49 Lamulo limeneli likhudza mbadwa ngakhalenso alendo wochita
mdulidwe wokhala pakati panu.

50 "Aisraeli onse anachita monga momwe Yehova analamulira Mose ndi
Aaroni. 51 Ndipo tsiku lomwelo Yehova anatulutsa gulu lonse la ana a
Israeli m'dziko la Igupto."

# 13

*Mwambo Wopatula Ana Oyamba Kubadwa*

1 Yehova anati kwa Mose, 2 "Ana onse aamuna oyamba kubadwa
uwapatule, ndi anga. Aliyense woyamba kubadwa pakati pa Aisraeli ndi
wanga, kaya ndi wa munthu kapena wa chiweto."

3 Ndipo Mose anati kwa anthu, "Muzikumbukira tsiku lino, tsiku
limene munatuluka m'dziko la Igupto, dziko la ukapolo chifukwa Yehova
anakutulutsani ndi dzanja lake lamphamvu. Musadye kalikonse kamene
kali ndi yisiti. 4 Pa tsiku la lero mwezi uno wa Abibu, mukutuluka
m'dziko la Igupto. 5 Yehova akadzakulowetsani m'dziko la Akanaani, Ahiti,
Aamori, Ahivi ndi Ayebusi, dziko loyenda mkaka ndi uchi, muzikachita
mwambo uwu mwezi uno. 6 Muzidzadya buledi wopanda yisiti kwa
masiku asanu ndi awiri ndipo tsiku lachisanu ndi chiwirilo muzichita
chikondwerero cha Yehova. 7 Mudye buledi wopanda yisiti masiku asanu
ndi awiri. Pasapezeke chinthu chilichonse chokhala ndi yisiti pakati panu,
kapena paliponse m'dziko lanu. 8 Tsiku limenelo muzidzawuza ana anu
kuti, 'Ine ndimachita zimenezi chifukwa cha zimene Yehova anandichitira
pamene ndimatuluka m'dziko la Igupto.' 9 Lamulo ili lidzakhala ngati
chizindikiro chomangidwa pa dzanja lanu ndi chikumbutso choyikidwa
pamphumi panu kuti malamulo a Yehova asachoke pakamwa panu. Pakuti
Yehova anakutulutsani m'dziko la Igupto ndi dzanja lake lamphamvu.
10 Muzichita mwambo uwu pa nthawi yake chaka ndi chaka.

11 "Yehova akadzakulowetsani ndi kukupatsani dziko la Kanaani monga
analonjezera kwa inu ndi makolo anu, 12 muzikapereka kwa Ambuye ana
onse oyamba kubadwa. Ziweto zonse zazimuna zoyamba kubadwa ndi
za Ambuye. 13 Koma mwana woyamba kubadwa wa bulu muzikamu-
wombola ndi mwana wankhosa, koma ngati simukamuwombola, muzika-
muthyola khosi. Mwana wamwamuna woyamba kubadwa muzikamu-
wombola.

14 “M’tsogolomo mwana wanu akakafunsa kuti, ‘Zimenezi zikutan-
thauza chiyani?’ Mukamuwuze kuti, ‘Yehova anatitulutsa m’dziko la
Igupto, dziko la ukapolo ndi dzanja lamphamvu. 15 Farao atakanitsitsa
kuti asatitulutse, Yehova anapha aliyense woyamba kubadwa m’dziko
la Igupto, kuyambira ana a anthu ndi ziweto zomwe. N’chifukwa
chake ine ndimapereka nsembe kwa Yehova, chachimuna chilichonse
choyamba kubadwa ndipo mwana wamwamuna woyamba kubadwa
ndimamuwombola.’ 16 Ndipo chidzakhala kwa inu ngati chizindikiro
chomangidwa pa dzanja lanu ndi pamphumi panu kuonetsa kuti Yehova
anakutulutsani m’dziko la Igupto ndi dzanja lake lamphamvu.”

### *Kuwoloka Nyanja*

17 Farao atalola anthu aja kuti atuluke, Mulungu sanawadzeretse njira
yodutsa dziko la Afilisti, ngakhale kuti inali yachidule popeza Mulungu
anati, “Ngati anthuwa atadzakumana ndi nkhondo angadzakhumudwe
ndi kubwerera ku Igupto.” 18 Choncho Mulungu anawadzeretsa anthuwo
njira yozungulira ya m’chipululu kulowera ku Nyanja Yofiira. Komabe
Aisraeli anatuluka m’dziko la Igupto atakonzekera nkhondo.

19 Mose ananyamula mafupa a Yosefe chifukwa Yosefe anawalumbiritsa
ana a Israeli. Iye anawawuza kuti, “Mulungu adzabwera ndithu kudza-
kuthandizani, ndipo mudzanyamule mafupa anga pochoka ku malo ano.”

20 Atachoka ku Sukoti anakagona ku Etamu m’mphepete mwa chipululu.
21 Nthawi yamasana Yehova amakhala patsogolo pa anthu kuwatsogolera
njira ndi chipilala cha mtambo, ndipo usiku Yehova ankawatsogolera ndi
chipilala cha moto, kuwawunikira njira kuti athe kuyenda masana ndi
usiku. 22 Usana, chipilala cha mtambo ndi usiku, chipilala cha moto zinali
patsogolo kuwatsogolera anthu aja.

## 14

1 Kenaka Yehova anati kwa Mose, 2 “Uza Aisraeli abwerere ndi kukagona
pafupi ndi Pihahiroti, pakati pa Migidoli ndi nyanja. Inu mumange
zithando m’mbali mwa nyanja moyang’anana ndi Baala-Zefoni. 3 Farao
adzaganiza kuti ‘Aisraeli asokonezeka n’kumangozungulirazungulira mu
dzikomo, chipululu chitawazinga.’ 4 Ndidzawumitsa mtima wa Farao
ndipo adzathamangira Aisraeliwo. Choncho ndikadzagonjetsa Farao ndi
gulu lake lonse la nkhondo, Ine ndidzalemekezedwa.” Choncho Aisraeli
aja anachita zimenezi.

5 Farao, mfumu ya Igupto atamva kuti anthu aja athawa, iye pamodzi
ndi nduna zake anasintha maganizo awo pa Israeli ndipo anati, “Ife
tachita chiyani? Tawalola Aisraeli kuti apite ndi kuleka kutitumikira?”
6 Choncho anakonzetsa galeta lake ndipo ananyamuka pamodzi ndi
ankhondo ake. 7 Iye anatenga magaleta 600 abwino kwambiri pamodzi ndi
magaleta ena a dziko la Igupto. Anatenganso akuluakulu onse ankhondo.
8 Yehova anawumitsa mtima wa Farao mfumu ya dziko la Igupto, kotero
iye anawathamangira Aisraeli amene ankachoka m’dzikomo mosavutika.
9 Aigupto aja (kutanthauza akavalo ndi magaleta onse a Farao, okwera
akavalowo pamodzi ndi gulu lonse la nkhondo) analondola Aisraeli aja
ndipo anakawapeza pamalo pamene anamanga zithando paja, m’mbali
mwa nyanja, pafupi ndi Pihahiroti, moyang’anana ndi Baala-Zefoni.

10 Tsono Farao anayandikira. Ndipo Aisraeli ataona kuti Aigupto
akuwatsatira, anachita mantha aakulu ndipo anafuwula kwa Yehova.

11 Iwo anafunsa Mose kuti, “Kodi n’chifukwa chakuti kunalibe manda
ku dziko la Igupto kuti iwe utibweretse muno m’chipululu kuti tidzafe?
Chimene watichitachi n’chiyani, kutitulutsa m’dziko la Igupto? 12 Kodi
sindizo zimene tinakuwuza m’dziko la Igupto? Ife tinati, ‘Tileke titu-
mikire Aigupto?’ Zikanatikomera kutumikira Aigupto kulekana ndi kufa
m’chipululu muno.”

13 Mose anayankha anthu kuti, “Musachite mantha. Imani, ndipo
muone chipulumutso chimene Yehova akuchitireni lero. Aigupto amene
mukuwaona lerowa simudzawaonanso. 14 Yehova adzakumenyerani
nkhondo. Inu mungokhala chete.”

15 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Chifukwa chiyani ukufuwulira
kwa ine? Uwuze Aisraeli aziyenda. 16 Nyamula ndodo yako ndi
kutambasula dzanja lako kuloza ku nyanja, kugawa madzi kuti Aisraeli
awoloke powuma. 17 Ine ndidzawumitsa mitima ya Aigupto kotero kuti
adzatsatirabe Aisraeli. Ndipo ine ndikadzagonjetsa Farao ndi asilikali
ake onse ankhondo, okwera magaleta ndi akavalo, ndidzapeza ulemerero.
18 Aigupto adzadziwa kuti Ine ndine Yehova akadzaona mmene ndipam-
banire Farao ndi magaleta ndi owayendetsa ake.”

19 Ndipo mngelo wa Mulungu amene amayenda patsogolo pa gulu
lankhondo la Israeli anachoka ndi kupita kumbuyo kwawo. Chipilala cha
mtambo chinasunthanso kuchoka kutsogolo ndi kupita kumbuyo kwawo.
20 Choncho mtambowo unakhala pakati pa asilikali ankhondo a dziko la
Igupto ndi a dziko la Israeli. Choncho panali mdima motero kuti magulu
awiri ankhondowa sanathe kuyandikizana usiku wonse.

21 Kenaka Mose anatambalitsa dzanja lake pa nyanja, ndipo Yehova
pogwiritsa ntchito mphepo yamphamvu ya kummawa imene inawomba
usiku wonse anabweza madzi ndi kuwumitsa nyanja ija. Choncho nyanja
ija inagawanika. 22 Ndipo Aisraeli anawoloka pakati pa nyanja powuma,
madzi atasanduka khoma kumanja ndi kumanzere kwawo.

23 Aigupto onse, Farao, ndi onse okwera pa magaleta ndi akavalo
anawalondola ndipo analowa m’madzi. 24 Kutatsala pang’ono kucha,
Yehova ali mu chipilala chamoto ndi chamtambo, anayang’ana asi-
likali ankhondo a Igupto ndipo anabweretsa chisokonezo pakati pawo.
25 Yehova anamanga matayala a magaleta kotero kuti ankavutika kuyenda.
Ndipo Aigupto anati, “Tiyeni tiwathawe Aisraeli! Yehova akuwamenyera
nkhondo kulimbana nafe.”

26 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Tambasula dzanja lako pa nyanja
kuti madzi amize Aigupto ndi magaleta awo ndi okwera pa akavalo.”
27 Mose anatambasula dzanja lake pa nyanja, ndipo mmene kumacha
nyanja inabwerera m’malo mwake. Aigupto pothawa anakumana nayo,
ndipo Yehova anawakokera m’nyanja momwemo. 28 Madzi anabwerera
ndi kumiza magaleta ndi okwera akavalo, asilikali ankhondo onse
amene anatsatira Aisraeli m’nyanja, palibe ndi mmodzi yemwe amene
anapulumuka.

29 Koma Aisraeli aja anawoloka nyanja pansi pali powuma, madzi
atachita khoma kumanja ndi kumanzere kwawo. 30 Tsiku limeneli Yehova
anapulumutsa Israeli m’manja mwa Aigupto ndipo Israeli anaona Aigupto
ali lambalamba m’mbali mwa nyanja atafa 31 Choncho Aisraeli anaona
dzanja lamphamvu la Yehova limene linagonjetsa Aigupto aja, ndipo iwo
anaopa Yehova ndi kumukhulupirira pamodzi ndi mtumiki wake Mose.

# 15

*Nyimbo ya Mose ndi Miriamu*

1 Ndipo Mose ndi Aisraeli anayimbira Yehova nyimbo iyi:
"Ine ndidzayimbira Yehova
pakuti wakwezeka m'chigonjetso.
Kavalo ndi wokwera wake,
Iye wawaponya m'nyanja.
2 Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga;
ndiye chipulumutso changa.
Iye ndiye Mulungu wanga, ndipo ndidzamutamanda,
Mulungu wa makolo anga, ine ndidzamukweza.
3 Yehova ndi wankhondo;
Yehova ndilo dzina lake.
4 Magaleta a Farao ndi asilikali ake ankhondo
Iye wawaponya m'nyanja.
Akatswiri ankhondo amphamvu a Farao
amizidwa m'Nyanja Yofiira.
5 Nyanja yakuya inawaphimba;
Iwo anamira pansi ngati mwala."

6 Yehova, dzanja lanu lamanja
ndi laulemerero chifukwa cha mphamvu zake.
Ndithu Yehova, dzanja lanu lamanja
linaphwanya mdani.
7 Ndi ulemerero wanu waukulu,
munagonjetsa okutsutsani.
Inu munatumiza mkwiyo wanu waukulu;
ndipo unawapsereza ngati udzu.
8 Ndi mpweya wotuluka m'mphuno mwanu
madzi anawunjikana pamodzi.
Nyanja yakuya ija inasanduka
madzi owuma gwaa kufika pansi.

9 Mdaniyo anati,
"Ine ndidzawalondola, ndipo ndidzawagwira.
Ndidzagawa chuma chawo;
ndiye chokhumba changa chidzakwaniritsidwa.
Ine ndidzasolola lupanga langa,
ndi mkono wanga ndidzawawononga."
10 Koma Inu munawuzira mphepo yanu,
ndipo nyanja inawaphimba.
Iwo anamira ngati chitsulo
m'madzi amphamvu.

11 Ndithu Yehova, pakati pa milungu,
ndani afanana nanu? Inu amene muli woyera,
ndiponso wotamandika wolemekezeka,
chifukwa cha ntchito zanu,
zazikulu ndi zodabwitsa?
12 Munatambasula dzanja lanu lamanja
ndipo dziko linawameza.

13 Ndi chikondi chanu chosasinthika mudzatsogolera
anthu amene munawawombola.
Ndi mphamvu zanu munawatsogolera
ku malo anu woyera.
14 Anthu amitundu ina anamva za mbiriyi ndipo ananjenjemera ndi mantha,
mantha woopsa agwira anthu a dziko la Filisiti.
15 Tsopano mafumu a ku Edomu agwidwa ndi mantha aakulu,
otsogolera a dziko la Mowabu akunjenjemera ndi mantha,
ndipo anthu a ku Kanaani asungunuka ndi mantha.
16 Onse agwidwa ndi mantha woopsa.
Popeza anaona mphamvu zanu zazikulu,
iwo ayima chilili ngati mwala mpaka anthu anu,
Inu Yehova atadutsa;
inde mpaka atadutsa anthu amene munawagula.
17 Inu mudzawalowetsa ndi kuwakhazikitsa
pa phiri lanu.
Pa malo pamene Inu Yehova munawapanga kuti muzikhalapo;
malo wopatulika amene Inu Ambuye munawakonza ndi manja anu.
18 "Yehova adzalamula
mpaka muyaya."

19 Akavalo a Farao, magaleta ndi oyendetsa akavalo atalowa m'nyanja,
Yehova anawabwezera madziwo m'nyanja ndi kuwamiza, koma Aisraeli
anawoloka nyanjayo powuma. 20 Ndipo Miriamu mneneri wamkazi,
mlongo wa Aaroni anatenga zoyimbira ndipo akazi onse anamutsatira
pambuyo, akuyimba ndi zoyimbira ndi kuvina. 21 Miriamu anawayimbira
nyimbo iyi:
"Imbirani Yehova,
chifukwa iye wapambana.
Kavalo ndi wokwerapo wake
Iye wawamiza m'nyanja."

*Madzi a ku Mara ndi Elimu*

22 Ndipo Mose anatsogolera Israeli kuchoka ku nyanja yofiira ndi
kupita ku chipululu cha Suri. Anayenda m'chipululu masiku atatu
wosapeza madzi. 23 Ndipo anafika ku Mara. Koma sanathe kumwa madzi
akumeneko chifukwa anali owawa. (Ndi chifukwa chake malowo amatchedwa Mara). 24 Tsono anthu aja anadandaulira Mose ndi kumufunsa
kuti, "Kodi tikumwa chiyani?"

25 Ndipo Mose anapemphera kwa Yehova, ndipo Yehova anamuonetsa
kamtengo. Iye anakaponya m'madzimo ndipo madzi anakhala abwino.
Kumeneko Yehova anawayikira lamulo ndi maweruziro. Kumenekonso
Yehova anawayesa. 26 Yehova anati, "Ngati inu mudzamvetsa bwino
mawu anga, kuchita zolungama, kumvera malamulo anga ndi kusamalitsa zimene ndikukuwuzani ndiye kuti Ine sindidzayika pa inu matenda amene ndinayika pa anthu a ku Igupto popeza ndine Yehova amene ndimakuchiritsani."

27 Kenaka anafika ku Elimu, kumene kunali akasupe khumi ndi awiri
ndi mitengo ya migwalangwa makumi asanu ndi awiri, ndipo anamanga misasa yawo kumeneko pafupi ndi madzi.

# 16

*Mana ndi Zinziri*

1 Pambuyo pake gulu lonse la Aisraeli linachoka ku Elimu, ndipo
pa tsiku la khumi ndi chisanu mwezi wachiwiri chichokere m'dziko la
Igupto, anafika ku chipululu cha Sini chimene chinali pakati pa Elimu ndi
Sinai. 2 M'chipululumo gulu lonse linadandaulira Mose ndi Aaroni 3 kuti,
"Kukanakhala bwino Yehova akanatiphera m'dziko la Igupto! Kumeneko
timadya nyama ndi buledi mpaka kukhuta, koma inu mwabwera nafe ku
chipululu kudzapha mpingo wonsewu ndi njala!"

4 Ndipo Yehova anati kwa Mose, "Ine ndidzakupatsani buledi wogwa
kuchokera kumwamba ngati mvula. Anthu azituluka tsiku lililonse
kukatola buledi wokwanira tsiku limenelo. Ine ndidzawayesa m'njira
imeneyi kuti ndione ngati adzatsatira malangizo anga. 5 Pa tsiku lachisanu
ndi chimodzi, pamene azidzakonza buledi amene abwera naye, adzapeza
kuti ndi wokwanira masiku awiri."

6 Kotero Mose ndi Aaroni anati kwa Aisraeli onse, "Nthawi yamadzulo
inu mudzadziwa kuti ndi Yehova amene anakutulutsani m'dziko la Igupto.
7 Ndipo mmawa mudzaona ulemerero wa Yehova pakuti wamva kudan-
daula kwanu. Kodi ife ndi yani kuti muzitidandaulira?" 8 Mose anati,
"Yehova adzakupatsani nyama madzulo aliwonse ndi buledi mmawa
uliwonse kuti mukhute chifukwa Iye wamva madandawulo anu. Nanga
ife ndi yani? Kudandaula kwanu simudandaulira ife, koma Yehova."

9 Kenaka Mose anawuza Aaroni kuti, "Uza gulu lonse la Aisraeli kuti,
'Bwerani pamaso pa Yehova pakuti wamva kudandaula kwanu.' "

10 Pamene Aaroni amayankhula ndi gulu lonse la Aisraeli, iwo
anayang'ana ku chipululu, ndipo ulemerero wa Yehova umaoneka mu
mtambo.

11 Yehova anati kwa Mose, 12 "Ine ndamva kudandaula kwa Aisraeli.
Awuze kuti, 'Madzulo mudzadya nyama ndipo mmawa mudzakhuta
buledi. Pamenepo mudzadziwa kuti ine ndine Yehova Mulungu wanu.' "

13 Madzulo amenewo panatuluka zinziri zimene zinali ponseponse pa
misasa yawo, ndipo mmawa panali mame kuzungulira misasa yawo.
14 Mamewo atachoka, pa nthaka m'chipululumo panaoneka tinthu tina
topyapyala komanso totuwa ngati chipale. 15 Aisraeli atationa anafunsana
wina ndi mnzake nati, "Kodi timeneti n'chiyani?" Popeza sanatidziwe.

Mose anawawuza kuti, "Uyu ndi buledi amene Yehova wakupatsani kuti
mudye. 16 Yehova walamula kuti, 'Aliyense atole zomukwanira kudya,
malita awiri pa munthu mmodzi molingana ndi chiwerengero cha anthu
amene ali mu tenti yanu.' "

17 Aisraeli anachita zonse anawawuza. Ena anatola zambiri ena
zochepa. 18 Ndipo iwo atayeza ndi muyeso wa malita awiri, iye
amene anatola zambiri sizinamutsalireko ndipo amene anatola pang'ono
sizinamuchepere. Aliyense anatola zomukwanira kudya.

19 Ndipo Mose anawawuza kuti, "Wina aliyense asasunge mpaka
mmawa."

20 Komabe ena sanamvere Mose, anasungako mpaka mmawa. Koma
mmawa mwake tonse tinali mphutsi zokhazokha. Kotero Mose
anawapsera mtima.

21 Mmawa uliwonse aliyense amatola zimene amazifuna, ndipo dzuwa
likatentha zimasungunuka. 22 Tsiku lachisanu ndi chimodzi anatuta
malita anayi munthu aliyense, ndipo atsogoleri a mpingo wonse anabwera
kudzawuza Mose za zimenezi. 23 Iye anawawuza kuti, "Izi ndi zimene
Yehova analamula, 'Mawa ndi tsiku lopumula, Sabata Loyera la Yehova,

choncho wotchani ndi kuphika zimene mukufuna. Sungani zotsala mpaka mmawa.' "

24 Choncho anasunga mpaka mmawa monga Mose anawalamulira,
ndipo sananunkhe kapena kuchita mphutsi. 25 Mose anati, "Idyani lero
chifukwa lero ndi Sabata la Yehova. Lero simukapeza chilichonse kunjaku.
26 Muzitola chakudya masiku asanu ndi limodzi koma tsiku la chisanu ndi
chiwiri ndi la Sabata, simukapeza chilichonse kunjaku."

27 Komabe anthu ena anapita kuti akatole chakudya tsiku lachisanu ndi
chiwiri, koma sanapeze kanthu. 28 Ndipo Yehova anafunsa Mose nati,
"Kodi inu muzipitirira kukana kusunga malamulo ndi malangizo anga
mpaka liti? 29 Taonani, popeza Yehova wakupatsani Sabata n'chifukwa
chake tsiku lachisanu ndi chimodzi amakupatsani chakudya cha masiku
awiri. Aliyense azikhala pamene ali pa tsiku lachisanu ndi chiwiri,
pasapezeke wotuluka kunja." 30 Kotero anthu anapuma tsiku lachisanu
ndi chiwiri.

31 Aisraeli anatchula chakudyacho Mana. Chakudyacho chinkaoneka
ngati mbewu zamapira, zoyera. Ndipo chinkakoma ngati chothira uchi.
32 Mose anati, "Chimene Yehova walamula ndi ichi: 'Tengani muyeso wa
malita awiri a mana ndi kusungira mibado imene ikubwera, kuti iwo adzaone chakudya chimene Ine ndinakupatsani kuti mudye m'chipululu pamene ndinakutulutsani m'dziko la Igupto.' "

33 Choncho Mose anati kwa Aaroni, "Tenga mtsuko ndipo uyikemo malita awiri a mana. Ndipo uyike manawo pamaso pa Yehova kusungira mibado imene ikubwera."

34 Monga momwe Yehova analamulira Mose, Aaroni anayika mtsuko
uja pafupi ndi bokosi la Chipangano kuti manawo asungike. 35 Aisraeli
anadya mana zaka 40, mpaka pamene anafika ku dziko kumene amati akakhazikeko. Iwo anadya mana mpaka pamene anafika m'malire a Kanaani.

36 (Malita awiri amafanana ndi gawo lakhumi la efa).

# 17

*Madzi Otuluka M'thanthwe*

1 Gulu lonse la Aisraeli linachoka ku chipululu cha Sini, ndi kumayenda malo ndi malo monga momwe anawalamulira Yehova. Iwo anamanga misasa yawo ku Refidimu koma kunalibe madzi woti anthu onse ndi
kumwa. 2 Kotero iwo anakangana ndi Mose nati, "Tipatse madzi akumwa."

Mose anayankha kuti, "Chifukwa chiyani mukukangana ndi ine? Chifukwa chiyani mukumuyesa Yehova?"

3 Koma anthu anali ndi ludzu pamenepo ndipo anang'ung'udza pamaso pa Mose namufunsa kuti, "Kodi n'chifukwa chiyani unatitulutsa m'dziko la Igupto kuti ife, ana athu pamodzi ndi ziweto zathu tife ndi ludzu?"

4 Ndipo Mose anapemphera kwa Yehova, "Kodi ndichite chiyani ndi anthu awa? Iwo atsala pang'ono kundigenda ndi miyala."

5 Yehova anati kwa Mose, "Pita patsogolo pa anthuwo. Tenga ndodo
imene unamenyera nyanja ya Nailo pamodzi ndi akuluakulu ena a Israeli
ndi kunyamuka. 6 Ine ndidzayima patsogolo pako pafupi ndi thanthwe la
ku Horebu. Ukamenye thanthwelo, madzi adzatuluka kuti anthu amwe."
Motero Mose anachita zimenezi pamaso pa akuluakulu a Israeli. 7 Ndipo
iye anatcha malowo Masa ndi Meriba chifukwa Aisraeli anakangana

ndi kuyesa Yehova ponena kuti, "Kodi pakati pathu pali Yehova kapena palibe?"

### *Aisraeli Agonjetsa Aamaleki*

8 Amaleki anabwera ku Refidimu kudzamenyana ndi Aisraeli. 9 Mose
anati kwa Yoswa, "Sankha amuna amphamvu ndipo upite ukamenyane
ndi Amaleki. Mawa ndidzayima pamwamba pa phiri nditagwira ndodo
ya Mulungu."
10 Ndipo Yoswa anachitadi monga Mose anamulamulira. Iye anapita
kukamenyana ndi Aamaleki ndipo Mose, Aaroni ndi Huri anapita
pamwamba pa phiri. 11 Mose ankati akakweza manja ake, Aisraeli ama-
pambana, koma akatsitsa manja akewo Amaleki amapambana. 12 Manja a
Mose atatopa, Aaroni ndi Huri anatenga mwala ndi kuyika pansi ndipo
Mose anakhalapo. Aaroni ndi Huri anagwirizitsa manja a Mose wina
mbali ina winanso mbali ina. Choncho manja a Mose analimba mpaka
kulowa kwa dzuwa. 13 Kotero Yoswa anagonjetsa asilikali ankhondo a
Amaleki ndi lupanga.
14 Kenaka Yehova anati kwa Mose, "Lemba izi m'buku kuti zidzakum-
bukirike ndipo uwonetsetse kuti Yoswa amve zimenezi, chifukwa Ine
ndidzafafaniziratu Amaleki pa dziko lapansi, kotero kuti palibe amene
adzawakumbukire."
15 Mose anamanga guwa lansembe ndipo analitcha Yehova Chipambano
Changa (Yehova Nisi). 16 Ndipo anati, "Kwezani mbendera ya Yehova.
Yehova adzachitabe nkhondo ndi mibado yonse ya Aamaleki."

## 18

### *Yetero Abwera Kudzaona Mose*

1 Yetero wansembe wa ku Midiyani amenenso anali mpongozi wa Mose,
anamva zonse zimene Mulungu anachitira Mose ndi anthu ake a Aisraeli
ndi mmene Yehova anawatulutsira m'dziko la Igupto.
2 Mose atamubweza Zipora, mkazi wake, Yetero, mpongozi wake
anamulandira 3 mwana wake wamkaziyo pamodzi ndi ana ake aamuna
awiri. Mose anamupatsa mwana wachisamba dzina loti Geresomu popeza
anati, "Ndakhala mlendo m'dziko lachilendo." 4 Ndipo mwana wake
wachiwiri anamupatsa dzina loti Eliezara, pakuti anati, "Mulungu wa
makolo anga anali thandizo langa. Iye anandipulumutsa ku lupanga la
Farao."
5 Yetero, mpongozi wa Mose pamodzi ndi ana a Mose aamuna awiri
ndi mkazi wake anabwera kwa Mose ku chipululu pa phiri la Mulungu
kumene Mose anamanga misasa. 6 Yetero anali atatumiza uthenga kwa
Mose kuti, "Ine Yetero, mpongozi wako, ndikubwera ndi mkazi wako ndi
ana ake awiri."
7 Kotero Mose anatuluka kukakumana ndi mpongozi wake ndipo
anawerama ndi kupsompsona. Atalonjerana anakalowa mu tenti 8 Mose
anafotokozera mpongozi wake zonse zimene Yehova anamuchita Farao
ndi Aigupto chifukwa cha Israeli komanso zowawa zonse anakumana nazo
m'njira. Mose anafotokozanso momwe Yehova anawapulumutsira.
9 Yetero anakondwa kwambiri atamva zabwino zonse zimene Yehova
anachitira Aisraeli powapulumutsa m'dzanja la Aigupto. 10 Iye anati,
"Alemekezeke Yehova amene wakupulumutsani m'dzanja la Aigupto ndi
Farao. Wapulumutsanso anthuwa m'dzanja la Aigupto. 11 Tsopano
ndikudziwa kuti Yehova ndi wopambana milungu ina yonse, pakuti

anachita izi kwa amene ananyoza Israeli.” 12 Ndipo Yetero, mpongozi
wa Mose anapereka nsembe yopsereza ndi nsembe zina kwa Mulungu.
Aaroni ndi akuluakulu onse a Israeli anabwera kudzadya chakudya
pamodzi ndi mpongozi wa Mose pamaso pa Mulungu.

13 Mmawa mwake, Mose anakhala pa mpando kuti aweruze milandu
ya anthu. Anthu anayima momuzungulira kuyambira mmawa mpaka
madzulo. 14 Mpongozi wa Mose ataona zonse zimene iye amawachitira
anthu anati, “N’chiyani chimene mukuwachitira anthuwa? N’chifukwa
chiyani mulipo nokha woweruza, pamene anthu onsewa ayimirira kuyambira mmawa mpaka madzulo?”

15 Mose anamuyankha kuti, “Chifukwa anthuwa anabwera kwa ine
kudzafunsa zimene Mulungu akufuna. 16 Ngati munthu akangana ndi
m’bale wake, onse awiri amabwera kwa ine, ndipo ine ndimawaweruza.
Ndimawawuzanso malamulo a Mulungu ndi malangizo ake.”

17 Mpongozi wa Mose anayankha kuti, “Zimene mukuchitazi si zabwino.
18 Ntchitoyi ndi yayikulu kuposa mphamvu zanu. Inu simungathe
kuyigwira nokha. Inu pamodzi ndi anthuwa amene amabwera kwa
inu mudzatopa. 19 Tsono tamverani ndikulangizeni, ndipo Mulungu
akhale nanu. Inu muziwayimirira anthuwa pamaso pa Mulungu, ndipo
mikangano yawo muzibwera nayo kwa Iye. 20 Aphunzitseni mawu ndi
malangizo a Mulungu. Aphunzitseni mmene ayenera kukhalira ndi
zimene ayenera kuchita. 21 Koma sankhani amuna odziwa ntchito yawo,
anthu owopa Mulungu, anthu odalirika amene amadana ndi kupeza
phindu mwachinyengo. Tsono muwayike kuti akhale oyang’anira anthu
motere: atsogoleri a anthu 1,000, ena a anthu 100, ena a anthu 50 ndi ena a
anthu khumi. 22 Tsono amenewa aziweruza anthu nthawi zonse. Mlandu
uliwonse waukulu azibwera nawo kwa inu, koma mlandu waung’ono
aziweruza okha. Izi zidzachititsa kuti ntchito yanu ipepuke, popeza
mudzagwira ntchito mothandizana. 23 Ngati mutsatira malangizowa
monga mmene Mulungu wakulamulirani ndiye kuti simudzafowoka ndipo
anthu onsewa adzapita kwawo mu mtendere.”

24 Mose anamvera mpongozi wake ndi kuchita zonse zimene iye
ananena. 25 Iye anasankha amuna odziwa bwino ntchito zawo ndipo
anawayika kuti akhale atsogoleri, oyang’anira anthu motere: atsogoleri
a anthu 1,000, ena a anthu 500, ena a anthu makumi asanu ndi ena a
anthu khumi. 26 Iwowa ankaweruza anthu nthawi zonse. Milandu yovuta
ankabwera nayo kwa Mose, koma yosavuta ankayiweruza okha.

27 Kenaka Mose analola kuti mpongozi wake, Yetero anyamuke kubwerera ku dziko la kwawo.

# 19

*Pa Phiri la Sinai*

1 Ana a Israeli aja anafika ku chipululu cha Sinai pa tsiku loyamba la
mwezi wachitatu chichokere m’dziko la Igupto. 2 Atachoka ku Refidimu,
anafika ku Sinai, ndipo Aisraeli anamangako misasa yawo moyang’anana
ndi phirilo.

3 Mose anakwera ku phiri kukakumana ndi Mulungu ndipo Yehova
anamuyitana nati, “Ukawuze zidzukulu za Yakobo, ana onse a Israeli
kuti, 4 ‘Inu eni munaona zimene ndinawachitira Aigupto ndiponso mmene
ndinakunyamulirani, monga mmene chiwombankhanga chimanyamulira
ana ake pa mapiko,’ ndikukubweretsani kwa Ine. 5 Tsopano, ngati

mumveradi mawu anga ndi kusunga pangano langa, mudzakhala chuma
changa chapamtima pakati pa mitundu yonse. Ngakhale kuti dziko lonse
lapansi ndi langa, 6 inu mudzakhala ansembe achifumu ndi mtundu
woyera mtima. Awa ndi mawu amene uyenera kuwawuza Aisraeli.”
7 Ndipo Mose anabwerera ndi kuyitanitsa akuluakulu. Atabwera
anawafotokozera mawu amene Yehova anamulamulira kuti adzanene.
8 Anthu onse anayankha pamodzi kuti, “Ife tidzachita zonse zimene
Yehova wanena.” Choncho Mose anabweza yankho lawo kwa Yehova.
9 Yehova anati kwa Mose, “Ine ndibwera kwa iwe mu mtambo
wakuda kuti anthu adzandimve ndikuyankhula ndi iwe. Choncho
adzakukhulupirira nthawi zonse.” Kenaka Mose anawuza Yehova zimene
anthu ananena.
10 Ndipo Yehova anati kwa Mose, “Pita kwa anthu onse ndi kuwayeretsa
lero ndi mawa. Achape zovala zawo 11 ndipo akhale atakonzeka pofika
tsiku lachitatu, chifukwa tsiku limenelo Yehova adzatsika pa phiri la Sinai
anthu onse akuona. 12 Uwalembere malire anthuwo kuzungulira phirilo
ndipo uwawuze kuti, ‘Samalani musakwere phirilo kapena kukhudza
tsinde lake. Aliyense wokhudza phiri adzaphedwa ndithu. 13 Aliyense
wokhudza phiri adzaphedwa ndi miyala kapena kumulasa ndi mivi.
Palibe amene adzamukhudze. Palibe munthu amene adzaloledwa kukhala
ndi moyo ngakhale nyama. Iwo adzayenera kuphedwa.’ Koma anthu
adzapita ku phirilo akadzamva kulira kwa lipenga la nyanga yankhosa.”
14 Tsono Mose anatsika phiri lija nafika kwa anthu aja ndi kuwayeretsa.
Iwo anachapa zovala zawo. 15 Kenaka iye anati kwa anthu, “Konzekerani
tsiku lachitatu, musagone pamodzi ndi mkazi.”
16 M’mamawa wa tsiku lachitatu kunali mabingu, ziphaliwali ndi
mtambo wakuda umene unaphimba phiri, ndiponso lipenga lolira
kwambiri. Aliyense ku misasa kuja ananjenjemera ndi mantha. 17 Ndipo
Mose anatsogolera anthu kutuluka m’misasa kukakumana ndi Mulungu,
ndipo anayima m’munsi mwa phiri. 18 Phiri la Sinai linakutidwa ndi
utsi, chifukwa Yehova anatsika ndi moto pa phiripo. Utsi unakwera ngati
wochokera m’ng’anjo yamoto ndipo phiri lonse linagwedezeka kwambiri.
19 Liwu la lipenga linkakulirakulira. Tsono Mose anayankhula ndipo
Yehova anamuyankha ndi mabingu.
20 Yehova anatsika nafika pamwamba pa phiri la Sinai, ndipo anayitana
Mose kuti apite pa phiripo. Choncho Mose anakwera, 21 ndipo Yehova
anati kwa iye, “Tsika ukawachenjeze anthu kuti asayesere kudutsa malire
kuti adzandione chifukwa ambiri a iwo adzafa. 22 Ngakhale ansembe
amene amatumikira pamaso pa Yehova ayenera kudziyeretsa kuopa kuti
ndingadzawalange.”
23 Mose anati kwa Yehova, “Anthu sangakwere phiri la Sinai chifukwa
inu munatichenjeza. Lembani malire kuzungulira phiri ndipo mulipatule
kuti likhale loyera.”
24 Yehova anayankha, “Tsika ukamutenge Aaroni. Koma ansembe ndi
anthu asayesere kubzola malire kuti abwere kwa Yehova chifukwa Iye
adzawalanga.”
25 Ndipo Mose anatsika ndi kukawawuza anthuwo.

# 20

*Malamulo Khumi*

1 Ndipo Mulungu anayankhula mawu onse awa nati:

2 “Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakutulutsa ku Igupto, m’dziko la ukapolo.

3 “Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha.”

4 “Usadzipangire chofanizira chinthu chilichonse chakumwamba kapena cha pa dziko lapansi kapena cha m’madzi a pansi pa dziko.
5 Usazigwadire kapena kuzipembedza, pakuti Ine Yehova Mulungu wako, ndine Mulungu wansanje, wolanga ana chifukwa cha tchimo la makolo awo mpaka m’bado wachitatu ndi wachinayi wa iwo amene
amadana nane. 6 Koma ndimaonetsa chikondi chosasinthika ku mibado miyandamiyanda ya anthu amene amandikonda, ndi kusunga malamulo anga.

7 “Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako, pakuti Yehova adzamutenga kukhala wochimwa aliyense amene akugwiritsa ntchito dzina lakelo molakwika.

8 “Uzisunga tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika. 9 Uzigwira
ntchito zako zonse masiku asanu ndi limodzi. 10 Koma tsiku
lachisanu ndi chiwiri ndi Sabata, tsiku loperekedwa kwa Yehova Mulungu wako. Tsiku limeneli musagwire ntchito iliyonse, inuyo kapena mwana wanu wamwamuna kapena mwana wanu wamkazi, wantchito wanu wamwamuna kapena mdzakazi wanu, ziweto zanu
kapena mlendo amene akukhala m’mudzi mwanu. 11 Pakuti Yehova
anapanga kumwamba ndi dziko lapansi, nyanja ndi zonse zimene zili m’menemo m’masiku asanu ndi limodzi. Iye anapuma pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Kotero Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale loyera.

12 “Lemekeza abambo ako ndi amayi ako kuti ukhale ndi moyo wautali m’dziko limene Yehova Mulungu wako akukupatsa.

13 “Usaphe.

14 “Usachite chigololo.

15 “Usabe.

16 “Usapereke umboni womunamizira mnzako.

17 “Usasirire nyumba ya mnzako. Usasirire mkazi wa mnzako kapena wantchito wake wamwamuna kapena mdzakazi wake, ng’ombe yake kapena bulu wake, kapena chilichonse cha mnzako.”

18 Pamene anthu ankamva mabingu ndi kuona ziphaliwali ndi kumvanso lipenga ndi kuona utsi umene umafuka m’phiri, ananjenjemera
ndi mantha. Ndipo iwo anayima patali. 19 Ndipo anati kwa Mose, “Iwe
utiyankhule ndipo tidzamvera. Koma usalole kuti Mulungu atiyankhule, tingafe.”

20 Koma Mose anati kwa anthuwo, “Musachite mantha. Mulungu wabwera kudzakuyesani kuti mukhale ndi mtima woopa Mulungu kuti musamuchimwire.”

21 Anthu aja anayima patali koma Mose anayandikira mtambo wakuda kumene kunali Mulungu.

### *Za Mafano ndi Maguwa Ansembe*

22 Ndipo Yehova anati kwa Mose, “Awuze izi Aisraeli: ‘Inu mwaona
nokha kuti Ine ndakuyankhulani kuchokera kumwamba. 23 Choncho
musadzipangire milungu yasiliva kapena yagolide kuti muziyipembedza pamodzi ndi Ine.’ ”

24 Mundimangire guwa ladothi ndipo muziperekapo nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano, nkhosa, mbuzi ndi ng’ombe zanu. Pamalo

paliponse pamene Ine ndidzakonza kuti muzinditamandirapo, ndidz-
abwera ndi kukudalitsani. 25 Ngati mudzandimangira guwa lansembe
lamiyala, musagwiritse ntchito miyala yosema, pakuti mudzalidetsa
mukadzagwiritsa ntchito zida. 26 Musamakwere pa makwerero popita pa
guwa langa lansembe kuti mungaonetse maliseche anu.

# 21

1 “Uwawuze Aisraeli malamulo awa:

### *Antchito a Chihebri*

2 “Mukagula kapolo wa Chihebri, azikugwirirani ntchito zaka zisanu ndi
chimodzi. Koma m’chaka cha chisanu ndi chiwiri muzimumasula, ndipo
asalipire kanthu. 3 Ngati anabwera yekha, amasulidwenso yekha. Koma
ngati anali ndi mkazi pamene ankabwera, mkaziyo apite nayenso. 4 Ngati
bwana wake amupatsa mkazi ndipo mkaziyo anabereka ana aamuna
kapena aakazi, mkazi ndi anawo adzakhala a bwanayo ndipo mwamuna
yekhayo ndiye adzamasulidwe.

5 “Koma ngati kapoloyo alengeza kuti, ‘Ine sindikufuna kumasulidwa
chifukwa ndimakonda mbuye wanga, mkazi wanga ndi ana,’ 6 mbuye
wakeyo abwere naye kwa Yehova. Abwere naye pa chitseko kapena pa
mphuthu zachitseko ndipo abowole khutu lake ndi chitsulo. Ndipo iye
adzakhala kapolo wake moyo wake wonse.

7 “Ngati munthu agulitsa mwana wake wamkazi kukhala mdzakazi,
mwanayo asamamasulidwe monga achitira ndi akapolo aamuna. 8 Koma
ngati mkaziyo sakukondweretsa bwana wake amene wamusankha kuti
amukwatire, amulole kuti awomboledwe. Bwanayo alibe mphamvu
zomugulitsa kwa anthu achilendo, chifukwa iyeyo waphwanya pangano
lake lomukwatira iye. 9 Ngati anamusankha kuti akhale mkazi wa mwana
wake, ayenera kumusunga ngati mwana wake wamkazi. 10 Ngati akwatira
mkazi wina, asamumane woyambayo chakudya ngakhale chovala ndipo
apiritirize kugona naye ngati mkazi wake. 11 Koma ngati sangathe
kumuchitira zonsezi, ndiye amuleke apite popanda kulipira kanthu.

### *Munthu Akapwetekedwa*

12 “Munthu aliyense amene amenya mnzake namupha, iyenso ayenera
kuphedwa. 13 Koma ngati sanachite dala, ndipo Mulungu analola kuti
zichitike, iyeyo athawire ku malo kumene ndidzakupatsani. 14 Koma
ngati munthu akonza chiwembu ndi kupha mnzake mwadala, ameneyo
muchotseni ngakhale ku guwa langa lansembe ndipo aphedwe.

15 “Munthu aliyense amene amenya abambo ake kapena mayi ake
ayenera kuphedwa.

16 “Munthu aliyense amene aba munthu mnzake, ndi kukamugulitsa,
kapena kumangomusunga, ayenera kuphedwa.

17 “Aliyense amene atemberera abambo ake kapena amayi ake ayenera
kuphedwa.

18 “Ngati anthu awiri akangana ndipo wina amenya mnzake ndi mwala
kapena nkhonya koma wosamupha, womenyedwayo akadwala nagona
pa bedi, 19 kenaka nachira ndi kuyamba kuyenda ndi ndodo kutuluka
kunja kwa nyumba yake, ndiye kuti womenya mnzakeyo sadzayimbidwa
mlandu. Komabe adzayenera kulipira womenyedwayo chifukwa cha

nthawi imene anagona pa bedi ija, ndiponso ayenera kumusala mpaka
atachiritsitsa.
[20] "Ngati munthu amenya kapolo wake wamwamuna kapena mdzakazi
ndi ndodo, kapolo uja ndikufa chifukwa cha kumenyedwako, munthuyo
ayenera kulangidwa. [21] Koma ngati kapolo uja akhala ndi moyo tsiku lonse
kapena masiku awiri, ndiye kuti mbuye uja asalangidwe chifukwa kapolo
ndi chuma chake.
[22] "Ngati anthu akumenyana ndi kupweteka mayi woyembekezera,
mayiyo napita padera, koma osavulala, wolakwayo ayenera kulipira chili-
chonse chimene mwamuna wake wa mkaziyo adzalamula ndipo bwalo
lamilandu lavomereza. [23] Koma ngati wavulazidwa kwambiri, ndiye
malipiro ake adzakhala motere: moyo kulipa moyo, [24] diso kulipira diso,
dzino kulipira dzino, mkono kulipa mkono, phazi kulipa phazi. [25] Kutentha
ndi moto kulipa kutentha ndi moto, bala kulipa bala, mkwingwirima
kulipa mkwingwirima.
[26] "Ngati munthu amenya wantchito wake wa mwamuna kapena
mdzakazi wake pa diso ndi kuliwononga, wantchitoyo amasulidwe
ngati malipiro a diso lake. [27] Ndipo ngati agulula dzino la wantchito
wamwamuna kapena mdzakazi, wantchitoyo amasulidwe ngati malipiro
a dzino lake.
[28] "Ngati ng'ombe ipha munthu wamwamuna kapena wamkazi ndi
nyanga yake, iponyedwe miyala ndipo nyama yake isadyedwe. Ndipo
mwini ng'ombeyo asayimbidwe mlandu. [29] Koma ngati ng'ombeyo inali
ndi chizolowezi chogunda anthu ndipo mwini wakeyo anachenjezedwa
koma iye sanayimange ndipo yapha mwamuna kapena mkazi, ng'ombeyo
iponyedwe miyala ndipo mwini wakeyo aphedwenso. [30] Koma ngati
wauzidwa kuti alipire, iye apereke zimene wauzidwazo kuti awombole
moyo wake. [31] Lamulo ili ligwirenso ntchito ngati ng'ombeyo yagunda
mwana wamwamuna kapena wamkazi. [32] Ngati ng'ombeyo yagunda
kapolo wamwamuna kapena mdzakazi, mwini ng'ombeyo apereke
masekeli makumi atatu a siliva kwa mwini kapoloyo, ndipo ng'ombeyo
iponyedwe miyala.
[33] "Munthu akasiya dzenje lapululu kapena akakumba dzenje koma
wosaphimbapo, ndipo ng'ombe kapena bulu n'kugweramo, [34] mwini dzen-
jelo amulipire mwini chiweto chakufacho koma iye atenge chiwetocho.
[35] "Ngati ng'ombe ya munthu wina ipha ng'ombe ya mnzake, ng'ombe
yamoyo ija igulitsidwe ndipo anthu awiriwo agawane pakati ndalama
yake. Achite chimodzimodzi ndi ng'ombe yakufa ija. [36] Koma zikadziwika
kuti ng'ombeyo inali ndi khalidwe logunda, ndipo mwini wake samay-
itsekera m'khola, mwini ng'ombeyo alipire ng'ombe ina yamoyo koma
atenge yakufayo."

## 22

*Za Kuteteza Katundu*

[1] "Ngati munthu aba ng'ombe kapena nkhosa ndi kuyipha kapena
kuyigulitsa, iye abweze ng'ombe zisanu pa ng'ombe imodzi ndi nkhosa
zinayi pa nkhosa imodzi.
[2] "Ngati mbala ipezeka ikuthyola nyumba ndipo imenyedwa n'kufa,
amene wapha mbalayo sanalakwe. [3] Koma akayipha dzuwa litatuluka,
woyiphayo ali ndi mlandu wakupha.

“Mbala iyenera kubweza ndithu koma ngati ilibe kalikonse igulitsidwe,
kulipira zomwe yabazo.

4 “Ngati chiweto chobedwacho chipezeka chamoyo m’manja mwake,
kaya ndi ng’ombe kapena bulu kapena nkhosa, mbalayo ibwezere ziweto
ziwiri pa chiweto chobedwacho.

5 “Ngati munthu alekerera ziweto zake kukalowa m’munda wa munthu
wina kukadya mbewu zake, munthuyo amubwezere mwini mundawo
mbewu zina zabwino kapena mpesa wina wabwino kwambiri.

6 “Ngati munthu ayatsa moto, motowo ndikukafika mpaka ku munda ndi
kuwotcha mulu wa tirigu kapena tirigu wosadula, kapena munda wonse,
ndiye kuti munthu amene anayatsa motoyo alipire.

7 “Ngati munthu asungitsidwa ndi mnzake ndalama kapena katundu,
ndipo zinthu zija n’kubedwa m’nyumba mwake, wakubayo ngati ag-
widwa, ayenera kubwezera kawiri chobedwacho. 8 Koma ngati mbalayo
sipezeka, mwini nyumbayo ayenera kukaonekera ku bwalo lamilandu
kuti akamve ngati anaba katundu wa mnzakeyo. 9 Ngati pali kukan-
gana kokhudza ng’ombe, bulu, nkhosa, zovala kapena kanthu kalikonse
kotayika, ndipo mmodzi ndikunena kuti chinthucho n’chake, awiriwo
abwere nawo mlandu wawowo pamaso pa Mulungu ndipo amene mlandu
umugomere adzayenera kumulipira mnzakeyo kawiri.

10 “Ngati munthu wina anasungitsa mnzake bulu, ng’ombe, nkhosa,
kapena chiweto chilichonse ndipo chiweto chija n’kufa kapena kup-
weteka kapena kutengedwa popanda wina kuona, 11 ndiye kuti anthu
awiriwo ayenera kulumbira pamaso pa Mulungu kuti asatenge chinthu
cha mnzake. Zikatero mwini katundu uja avomereze zimenezi ndipo
asabwezeredwe kanthu. 12 Koma ngati chiwetocho chinabedwa, iye
ayenera kubwezera mwini wakeyo. 13 Ngati chinagwidwa ndi zirombo,
iye ayenera kubweretsa zotsalira ngati umboni ndipo sadzalipira kanthu.

14 “Ngati munthu abwereka chiweto cha mnzake ndipo chiweto chija
n’kuvulala kapena kufa chikanali ndi iyebe, wobwerekayo ayenera
kulipira. 15 Koma ngati mwini wakeyo ali ndi chiwetocho, wobwerekayo
sadzalipira. Ngati anapereka ndalama pobwereka chiwetocho, ndalama
anaperekazo zilowa m’malo mwa chiweto chakufacho.

### *Malamulo a Kakhalidwe ka Anthu*

16 “Ngati munthu anyenga namwali wosadziwa mwamuna amene
sanapalidwe ubwenzi ndi kugona naye, munthuyo ayenera kulipira
malowolo ndipo adzakhala mkazi wake. 17 Ngati abambo ake akanitsitsa
kwamtuwagalu kumupereka kuti amukwatire, munthuyo aperekebe mal-
owolo woyenera namwaliyo.

18 “Musayilole mfiti yayikazi kuti ikhale ndi moyo.

19 “Aliyense wogonana ndi chiweto ayenera kuphedwa.

20 “Aliyense wopereka nsembe kwa mulungu wina osati Yehova
awonongedwe.

21 “Musazunze mlendo kapena kumuchitira nkhanza, pakuti inu munali
alendo m’dziko la Igupto.

22 “Musazunze mkazi wamasiye kapena mwana wamasiye. 23 Ngati
muwazunza ndipo iwo n’kulirira kwa Ine, ndidzamva kulira kwawo.
24 Ine ndidzakukwiyirani ndipo ndidzakuphani ndi lupanga. Akazi anu
adzakhala amasiye ndiponso ana anu adzakhala wopanda abambo.

25 “Ngati mukongoza ndalama kwa m’bale wanu amene ndi m’mphawi
pakati panu, musadzamuchite monga zimene amachita wokongoza

ndalama. Musadzamuyikire chiwongoladzanja. 26 Mukatenga chovala
cha mnzanu kuti chikhale chikole mumubwezere dzuwa lisanalowe
27 chifukwa chovala chimene amadzifundira nacho n'chomwecho. Nanga
usiku adzafunda chiyani? Tsonotu ngati adzandilirira, Ine ndidzamva
pakuti ndine wachifundo.

28 "Musachite chipongwe Mulungu wanu kapena kutemberera mtsogoleri wa anthu anu.

29 "Musachedwe kupereka kwa Ine zokolola zanu zochuluka ndi vinyo wanu wochuluka.

"Mundipatse ana anu achisamba aamuna. 30 Muchite chimodzimodzi
ndi ng'ombe zanu ndi nkhosa zanu. Mwana woyamba kubadwa azikhala ndi amayi ake masiku asanu ndi awiri. Koma pa tsiku lachisanu ndi chitatu mwanayo muzimupereka kwa Ine.

31 "Inu mukhale anthu anga opatulika. Choncho musadye nyama ya chiweto chimene chaphedwa ndi zirombo. Nyamayo muwaponyere agalu."

# 23

### *Malamulo a Zachilungamo ndi Zachifundo*

1 "Usafalitse mbiri yabodza. Usathandize munthu wolakwa pomuchitira umboni wonama.

2 "Usatsate gulu la anthu ndi kuchita choyipa. Pamene ukupereka
umboni m'bwalo lamilandu, usakhotetse mlandu chifukwa chofuna
kukondweretsa anthu ambiri. 3 Ndipo poweruza mlandu wa munthu
wosauka usamukondere.

4 "Ngati ukumana ndi ng'ombe kapena bulu wa mdani wako zitasochera,
uwonetsetse kuti wazitenga kupita nazo kwa mwini wakeyo. 5 Ngati
uwona bulu wa munthu wina amene amakuda atagwa ndi katundu, usamusiye pomwepo, uwonetsetse kuti wamuthandiza.

6 "Usakhotetse milandu ya anthu osauka. 7 Upewe zabodza ndipo
usaphetse munthu wosalakwa ndi wolungama, chifukwa Ine sindidzakhululukira wochimwa.

8 "Musamalandire chiphuphu, pakuti chiphuphu chimadetsa m'maso anthu oweruza ndi kusintha mawu awo kuti mlandu uyipire osalakwa.

9 "Usamuzunze mlendo, pakuti inu nomwe mukudziwa mmene amamvera mlendo chifukwa nanunso munali alendo m'dziko la Igupto.

### *Malamulo a Nthawi Zopuma*

10 "Muzidzala mbewu zanu m'munda ndi kumakolola mbewuzo kwa
zaka zisanu ndi chimodzi. 11 Koma chaka chachisanu ndi chiwiri muzisiya
osalima mindayo kuti anthu osauka pakati panu azipezamo chakudya, ndipo nyama zakuthengo zizidya zotsalazo. Muzichita chimodzimodzi ndi minda ya mpesa ndi mitengo ya olivi.

12 "Muzigwira ntchito masiku asanu ndi limodzi koma tsiku lachisanu ndi chiwiri musagwire ntchito kuti ng'ombe yanu ndi bulu wanu apume ndiponso kuti kapolo wobadwira m'nyumba yanu ndi mlendo yemwe apezenso mphamvu.

13 "Samalani pochita zonse zimene ine ndanena. Musamapemphere kwa milungu ina ndipo mayina awo musamawatchule.

### *Masiku Atatu Akulu a Chikondwerero*

14 "Muzichita zikondwerero zolemekeza Ine katatu pa chaka.

15 “Muzichita Chikondwerero cha Buledi wopanda Yisiti. Kwa masiku
asanu ndi awiri muzidya buledi wopanda yisiti monga ndinakulamulirani.
Muzichita zimenezi mwezi wa Abibu pa nthawi yomwe ndayika, pakuti
m’mwezi umenewu munatuluka m’dziko la Igupto.

“Pasapezeke munthu wobwera pamaso panga wopanda kanthu
m’manja.

16 “Muzichita Chikondwerero cha Masika pogwiritsa ntchito zipatso
zoyambirira kucha zimene munadzala m’munda.

“Muzichitanso Chikondwerero cha Zokolola pakutha pa chaka, pamene
mukututa zokolola zanu m’munda.

17 “Amuna onse azionekera pamaso pa Ambuye Yehova katatu pa chaka.

18 “Musapereke magazi anyama ngati nsembe kwa Ine pamodzi ndi
chilichonse chimene chili ndi yisiti.

“Ndipo musasunge mafuta anyama yansembe ya pa chikondwerero
mpaka mmawa.

19 “Muzibwera ndi zipatso zoyambirira kucha zabwino kwambiri ku
Nyumba ya Yehova Mulungu wanu.

“Musamaphike kamwana kambuzi mu mkaka wa mayi wake.

### *Kutsogolera kwa Mngelo wa Mulungu*

20 “Taona Ine ndikutuma mngelo wanga patsogolo panu kuti
akutetezeni m’njiramo ndi kukakufikitsani ku malo amene ndakonza.
21 Muzimumvera ndi kumvetsetsa zimene akunena. Musamuwukire
chifukwa sadzakhululuka kuwukira kwanu, pakuti akuchita zimenezi
m’dzina langa. 22 Ngati mudzamvera iyeyu ndi kuchita zonse zimene Ine
ndikunena, Ine ndidzakhala mdani wa adani anu ndipo ndidzatsutsana
ndi onse otsutsana nanu. 23 Mngelo wanga adzakhala patsogolo panu
ndipo adzakufikitsani m’dziko la Aamori, Ahiti, Aperezi, Akanaani, Ahivi
ndi Ayebusi, ndipo ndidzawapheratu onsewo. 24 Musagwadire milungu
yawo kapena kuyipembedza. Ndipo musatsatire zinthu zomwe amachita.
Koma inu mukawononge milungu yawo ndi kuphwasula malo amene
amapembedzerapo. 25 Muzipembedza Yehova Mulungu wanu ndipo
adzakudalitsani ndi chakudya ndi madzi ndiponso ndidzachotsa nthenda
pakati panu. 26 Palibe mkazi amene adzapite padera kapena kukhala
wosabereka m’dziko mwanu. Ndidzakupatsani moyo wautali.

27 “Ine ndidzawachititsa mantha ndi kusokoneza anthu onse amene
adzalimbana ndi inu ndipo adani anu onse adzakuthawani. 28 Ahivi,
Akanaani ndi Ahiti adzathawa ngati kuti ndawatumizira mavu. 29 Komabe
sindidzawachotseratu onse m’chaka chimodzi chifukwa dziko lingadza-
khale lopanda anthu ndipo nyama zakuthengo zidzakuchulukirani.
30 Ndidzawathamangitsa pang’onopang’ono mpaka inu mutachuluka kok-
wanira mwakuti n’kutenga dzikolo.

31 “Malire a dziko lanu adzakhala kuyambira ku Nyanja Yofiira mpaka
ku nyanja ya Afilisti, ndiponso kuyambira ku chipululu mpaka ku mtsinje
wa Yufurate. Anthu onse okhala m’dziko limeneli ndidzawapereka
m’manja mwanu ndipo mudzawathamangitsa. 32 Musachite pangano
ndi iwo kapena ndi milungu yawo. 33 Asadzakhale m’dziko lanu chi-
fukwa angadzakuchimwitseni ndi kuyamba kupembedza milungu yawo.
Mukadzatero ndiye kuti mwakodwa mu msampha.”

# 24

*Kutsimikizira kwa Pangano*

1 Ndipo Yehova anati kwa Mose, "Bwera ku phiri kuno kwa Yehova,
iwe pamodzi ndi Aaroni, Nadabu, Abihu ndi akuluakulu a Israeli makumi
asanu ndi awiri. Enanu mundipembedze muli chapatali. 2 Koma Mose
yekha ayandikire Yehova, ndipo enawo asayandikire. Komanso anthu ena
onse asakwere nawe ku phiri kuno."

3 Tsono Mose anapita kukawuza anthu mawu onse a Yehova ndi mala-
mulo onse, ndipo anthu onse anayankha mogwirizana kuti, "Tidzachita
zonse zimene Yehova wanena." 4 Ndipo Mose analemba zonse zimene
Yehova ananena.

Mmawa mwake Mose anadzuka nayamba kumanga guwa lansembe
m'munsi mwa phirilo ndipo anayimika miyala khumi ndi iwiri ngati
zipilala kuyimira mafuko khumi ndi awiri a Israeli. 5 Kenaka Mose ana-
tuma Aisraeli achinyamata kuti aphe ndi kukapereka kwa Yehova nsembe
zopsereza zachiyanjano. 6 Mose anatenga theka la magazi ndi kuyika
m'mbale, ndipo theka linalo analiwaza pa guwa lansembe. 7 Anatenganso
Buku la Chipangano ndi kuwerengera anthu. Anthuwo anayankha kuti,
"Zonse zimene Yehova wanena tamva, ndipo tidzazichita."

8 Kenaka Mose anatenga magazi, nawaza anthuwo ndipo anati, "Awa ndi
magazi a pangano limene Yehova wapanga ndi inu molingana ndi mawu
ake onsewa."

9 Kenaka Mose pamodzi ndi Aaroni, Nadabu, Abihu ndi akuluakulu
makumi asanu ndi awiri a Israeli aja anakwera ku phiri, 10 ndipo anaona
Mulungu wa Israeli. Pansi pa mapazi ake panali njira yoyendamo
yopangidwa ndi mwala wa safiro woyalidwa bwino wa maonekedwe
owala ngati thambo. 11 Ngakhale anaona Yehova koma sanafe, m'malo
mwake anadya ndi kumwa.

12 Yehova anati kwa Mose, "Bwera kwa ine ku phiri kuno, ndipo
udikire konkuno. Ndidzakupatsa miyala imene ndalembapo malemba kuti
ndiwaphunzitse."

13 Ndipo anayamba ulendo wopita ku phiri la Mulungu pamodzi ndi
womuthandiza wake Yoswa. 14 Apa n'kuti Mose atawawuza akuluakulu
aja kuti, "Mudikire pano mpaka titabweranso. Aaroni ndi Huri ali nanu,
aliyense amene ali ndi milandu apite kwa iwo."

15 Mose atakwera ku phiri kuja mtambo unaphimba phirilo.
16 Ulemerero wa Yehova unakhala pa phiri la Sinai, ndipo mtambo
unaphimba phirilo kwa masiku asanu ndi limodzi. Pa tsiku lachisanu ndi
chiwiri Yehova anayitana Mose kuchokera mu mtambowo. 17 Ulemerero
wa Yehova uja unkaoneka ngati malawi a moto pamwamba pa phirilo.
18 Ndipo Mose analowa m'mitambo nakwera phiri. Iye anakhala ku
phiriko 40 usana ndi usiku.

# 25

*Zopereka Zomangira Chihema*

1 Yehova ananena kwa Mose kuti, 2 "Uza Aisraeli kuti abweretse chop-
ereka kwa Ine. Iwe ulandire choperekacho m'malo mwanga kuchokera
kwa munthu amene akupereka mwakufuna kwake. 3 Zopereka zimene
ulandire kwa anthuwo ndi izi: Golide, siliva ndi mkuwa. 4 Nsalu
zobiriwira, zapepo, zofiira, nsalu zofewa, ubweya wambuzi; 5 zikopa za

nkhosa zazimuna za utoto wofiira ndi zikopa za akatumbu; matabwa
amtengo wa mkesha; 6 mafuta anyale a olivi, zonunkhiritsa mafuta
odzozera ndi zopangira lubani wonunkhira; 7 miyala yokongola ya
mtundu wa onikisi ndi ina yabwino yoyika pa efodi ndi pa chovala cha
pachifuwa.

8 “Iwo andipangire malo wopatulika, ndipo Ine ndidzakhala pakati
pawo. 9 Umange chihema ndiponso ziwiya zam’katimo monga momwe
Ine ndidzakuonetsere.

### *Bokosi la Chipangano*

10 “Tsono apange bokosi lamatabwa amtengo wa mkesha, ndipo kuta-
lika kwake kukhale masentimita 114, mulifupi mwake masentimita 69,
msinkhu wake masentimita 69. 11 Bokosilo ulikute ndi golide wabwino
kwambiri, m’kati mwake ndi kunja komwe, ndipo upange mkombero
wagolide kuzungulira bokosilo. 12 Upange mphete zinayi zagolide ndipo
uzimangirire ku miyendo yake inayi ya bokosilo, mbali ina ziwiri ndi
mbali inanso ziwiri. 13 Kenaka upange mizati yamtengo wa mkesha ndi
kuzikuta ndi golide. 14 Ndipo ulowetse nsichizo m’mphete zija za mbali
zonse ziwiri za bokosilo kuti azinyamulira. 15 Nsichizo zizikhala m’mphete
za bokosilo nthawi zonse, zisamachotsedwe. 16 Ndipo udzayike m’bokosilo
miyala iwiri yolembedwapo malamulo imene Ine ndidzakupatse.

17 “Upange chivundikiro cha bokosilo cha golide wabwino kwambiri,
kutalika kwake masentimita 114, mulifupi mwake masentimita 69.
18 Ndipo upange Akerubi awiri agolide osula ndi nyundo, uwayike
mbali ziwiri za chivundikirocho, 19 kerubi mmodzi mbali ina ndi
wina mbali inayo. Akerubiwa uwapangire limodzi ndi chivundikirocho
m’mapeto mwa mbali ziwirizo. 20 Mapiko a Akerubiwo adzatambasukire
pamwamba pa chivundikiro cha bokosilo kuti achiphimbe. Akerubiwo
adzakhale choyang’anana, aliyense kuyang’ana chivundikirocho. 21 Uyike
chivundikirocho pamwamba pa bokosi ndipo m’bokosilo uyikemo miyala
ya malamulo, imene ndidzakupatse. 22 Ndizidzakumana nawe pamenepo,
pamwamba pa chivundikiro cha bokosilo, pakati pa Akerubi awiriwo,
ndikumadzakupatsa malamulo onse okhudzana ndi Aisraeli.

### *Tebulo la Buledi Woperekedwa kwa Mulungu*

23 “Upange tebulo la matabwa amtengo wa mkesha, mulitali mwake
masentimita 91, mulifupi mwake masentimita 46, msinkhu wake masen-
timita 69. 24 Tebulolo ulikute ndi golide wabwino kwambiri ndipo
upange mkombero wagolide m’mbali mwake. 25 Upange feremu yozun-
gulira tebulo, mulifupi mwake ngati chikhatho cha dzanja, ndipo uyike
mkombero wagolide kuzungulira feremuyo. 26 Upange mphete zinayi
zagolide, ndipo uzilumikize ku ngodya zake zinayi, kumene kuli miyendo
yake inayi. 27 Mphetezo uziyike kufupi ndi feremu kuti azikolowekamo
nsichi zonyamulira tebuloyo. 28 Upange nsichi zamtengo wa mkesha
ndi kuzikuta ndi golide kuti azinyamulira tebulolo. 29 Upange mbale
ndi zipande zagolide wabwino, pamodzinso ndi mitsuko ndi mabeseni
zogwiritsa ntchito popereka nsembe. 30 Pa tebulopo uyikepo buledi
woperekedwa kosalekeza, kuti azikhala pamaso panga nthawi zonse.

### *Choyikapo Nyale*

31 “Upange choyikapo nyale chagolide wabwino kwambiri. Tsinde
lake ndi mphanda zake zikhale zosulidwa ndi nyundo. Zikho zake
zokhala ndi mphukira ndi maluwa ake zipangidwire kumodzi. 32 M’mbali
mwake mukhale mphanda zisanu ndi imodzi, zitatu mbali iliyonse.
33 Zikho zitatu zokhala ngati za maluwa amtowo, mphukira ndi duwa
zikhale pa mphanda yoyamba. Pa mphanda yachiwiri pakhalenso
zikho zitatu zokhala ngati za maluwa amtowo, mphukira ndi duwa.
Ndipo mphanda zonse zisanu ndi imodzi zikhale chimodzimodzi ndipo
zituluke m’choyikapo nyalecho. 34 Pa choyikapo nyalecho pakhale zikho
zinayi zopangidwa ngati maluwa amtowo ali ndi mphukira ndi maluwa.
35 Mphukira yoyamba ikhale m’munsi mwa nthambi ziwiri zoyamba za pa
choyikapo nyale. Mphukira yachiwiri ikhale m’munsi mwa nthambi ziwiri
zinazo. Ndipo mphukira yachitatu ikhale m’munsi mwa nthambi zina
ziwirinso. Zonse pamodzi zikhale nthambi zisanu ndi imodzi 36 Mphukira
ndi nthambi zonse zisulidwe kumodzi ndi choyikapo nyalecho ndi golide
wabwino kwambiri.
37 “Ndipo upange nyale zisanu ndi ziwiri ndi kuziyika pa choyikapo
nyalecho kuti ziwunikire kutsogolo. 38 Mbaniro ndi zowolera phulusa
zikhale zagolide wabwino kwambiri. 39 Choyikapo nyale ndi zipangizo
zonse zipangidwe ndi golide wabwino kwambiri wolemera makilogalamu
34. 40 Uwonetsetse kuti wapanga zonse monga momwe ndikukuonetsera
pa phiri pano.”

# 26

*Chihema cha Mapemphero*

1 “Panga chihema pogwiritsa ntchito nsalu khumi zofewa, zosalala ndi
zolukidwa bwino, zobiriwira, zapepo ndi zofiira. Ndipo anthu aluso apete
pa nsaluzo Akerubi. 2 Nsalu zonse zikhale zofanana. Mulitali mwake
zikhale mamita khumi ndi atatu, mulifupi mamita awiri. 3 Ulumikize
nsalu zisanu kuti ikhale nsalu imodzi. Uchite chimodzimodzi ndi nsalu
zisanu zinazo. 4 Panga zokolowekamo za nsalu yobiriwira m’mphepete
mwa nsalu imodzi yotsiriza ya mbali ina. Uchitenso chimodzimodzi ndi
nsalu yotsiriza ya mbali inayo. 5 Upange zokolowekamo 50 pa nsalu
yoyamba ndi zokolowekamo makumi asanu zinanso pa nsalu inayo.
Upange motero kuti zokolowekamozo ziziyang’anana. 6 Kenaka upange
ngowe zagolide makumi asanu zolumikizira nsalu ziwirizo kuti zipange
chihema chimodzi.
7 “Upange nsalu za ubweya wambuzi zophimba pamwamba pa chi-
hemacho. Nsalu zonse pamodzi zikhale khumi ndi imodzi. 8 Nsalu
zonse khumi ndi imodzi zikhale zofanana. Mulitali mwake mukhale
mamita khumi ndi anayi ndipo mulifupi mwake mukhale mamita awiri.
9 Ulumikize nsalu zisanu kuti ikhale nsalu imodzi ndipo zina zisanu ndi
imodzi uzilumikizenso kuti ikhale nsalu imodzinso. Nsalu yachisanu
ndi chimodzi imene ili kutsogolo kwa tenti uyipinde pawiri. 10 Upange
zokolowekamo 50 m’mphepete mwa nsalu imodzi yotsirizira ya nsalu
yoyamba yolumikiza ija. Upangenso zokolowekamo zina 50 m’mphepete
mwa nsalu yotsirizira ya nsalu inanso yolumikiza ija. 11 Kenaka
upange ngowe 50 zamkuwa ndipo uzilowetse mu zokolowekazo. Ndiye
uphatikize nsalu ziwirizo kuti tentiyo ikhale imodzi. 12 Theka lotsalira
la nsaluyo lidzalendewera kumbuyo kwa chihemacho. 13 Nsalu yotsalira
ya masentimita 46 mulitali mwake m’mbali zonse ziwiri idzalendewere

kuphimba mbali ziwirizo. 14 Upange chikopa cha nkhosa zazimuna cha
utoto wofiira chophimbira tentiyo ndipo pamwamba pake upangireponso
chophimbira china cha zikopa za akatumbu.

15 “Upange maferemu amatabwa amtengo wa mkesha oyimikira chi-
hemacho. 16 Feremu iliyonse ikhale yotalika mamita anayi ndipo
mulifupi mwake mukhale masentimita 69. 17 Thabwa lililonse likhale
ndi zolumikizira ziwiri. Upange maferemu onse a chihemacho ndi
matabwa otere. 18 Upange maferemu makumi awiri a mbali yakummwera
kwa chihemacho. 19 Ndipo upange matsinde 40 asiliva ndipo uwayike
pansi pa maferemuwo. Pansi pa feremu iliyonse pakhale matsinde
awiri ogwiriziza zolumikizira ziwiri zija. 20 Ndipo mbali yakumpoto ya
chihemacho upangenso maferemu makumi awiri. 21 Upangenso matsinde
40 asiliva, awiri pansi pa feremu iliyonse. 22 Upange maferemu asanu
ndi imodzi a kumbuyo kwa tenti, kumbali yakumadzulo. 23 Ndipo
upangenso maferemu awiri a pa ngodya yakumbuyo kwenikweni kwa
tenti. 24 Pa ngodya ziwirizi pakhale maferemu awiri, kuyambira pansi
mpaka pamwamba ndipo alumikizidwe pa ngowe imodzi. Maferemu onse
akhale ofanana. 25 Choncho pakhale maferemu asanu ndi atatu ndiponso
matsinde 16 asiliva, awiri akhale pansi pa feremu iliyonse.

26 “Upange mitanda ya matabwa amtengo wa mkesha: mitanda isanu
ikhale ya maferemu a mbali imodzi ya chihema, 27 mitanda isanu inanso
ikhale ya maferemu a mbali inayo. Pakhalenso mitanda ina isanu ya mbali
yakumadzulo, kumapeto kwenikweni kwa chihema. 28 Mtanda wapakati
pa maferemuwo uchokere pa maferemu a mbali ina mpaka mbali inanso.
29 Maferemuwo uwakute ndi golide ndiponso upange mphete zagolide
zogwiriziza mitandayo. Ndipo mitandayonso uyikute ndi golide.

30 “Upange chihema mofanana ndi momwe ndinakuonetsera pa phiri
paja.

31 “Upange nsalu yokhala ndi mtundu wamtambo, wapepo ndi ofiira
ndipo nsaluyo ikhale yolukidwa bwino, yofewa ndi yosalala. Ndipo anthu
aluso apetepo zithunzi za Akerubi. 32 Nsaluyo uyikoloweke pa nsanamira
zinayi zamtengo wa mkesha zokutidwa ndi golide zomwe zili ndi ngowe
zagolide, zomwe zayima pa matsinde asiliva anayi. 33 Ukoloweke
kataniyo ku ngowe ndipo uyike Bokosi la Chipangano m’katimo. Kataniyo
idzalekanitse malo wopatulika ndi malo wopatulika kwambiri. 34 Uyike
chivundikiro pa bokosi laumboni ku malo wopatulika kwambiri. 35 Uyike
tebulo kunja kwa katani yotchinga cha kumpoto kwa chihema ndipo uyike
choyikapo nyale chija kummwera moyang’anana ndi tebulolo.

36 “Pa chipata cholowera mu chihema, uyikepo nsalu yamtundu
wamtambo, wapepo ndi ofiira, yomwe ndi yofewa ndi yosalala, yopet-
edwa bwino ndi amisiri aluso. 37 Upange ngowe zagolide za nsaluyo
ndi nsanamira zisanu zamtengo wa mkesha ndipo uzikute ndi golide.
Upangenso matsinde asanu amkuwa a nsanamirazo.”

# 27

*Guwa Lansembe Yopsereza*

1 “Upange guwa lansembe lamatabwa amtengo wa mkesha. Likhale
lofanana mbali zonse, msinkhu wake masentimita 137, mulitali mwake
masentimita 229, mulifupi mwake masentimita 229. 2 Upange nyanga

imodziimodzi pa ngodya zake zinayizo kuti nyangazo ndi guwalo zikhale
chinthu chimodzi, ndipo ulikute guwalo ndi mkuwa. [3] Upange ziwiya
zamkuwa izi zogwirira ntchito pa guwalo: miphika yochotsera phu-
lusa, mafosholo, mabeseni owazira magazi, ngowe zokowera nyama
ndi zosonkhezera moto. [4] Upange sefa yachitsulo chamkuwa ndipo
m'ngodya zake zinayizo upangiremo mphete zamkuwa. [5] Uyike sefayo
mmunsi mwa khoma la guwa lansembelo, ndipo ilekezere pakati pa
guwa lansembelo. [6] Upange nsichi zamtengo wa mkesha ndipo uzikutire
ndi mkuwa. [7] Pamene mukunyamula guwalo, muzilowetsa nsichizo
m'mphetemo mbali zonse ziwiri za guwalo. [8] Guwalo likhale lamatabwa
ndi logoba m'kati mwake. Ulipange monga momwe ndinakuonetsera pa
phiri paja.

### *Za Bwalo la Chihema*

[9] "Upange bwalo la chihema. Mbali yakummwera ikhale yota-
lika mamita 46 ndipo ikhale ndi nsalu yotchinga yofewa yosalala
yolukidwa bwino. [10] Upangenso mizati makumi awiri, matsinde
makumi awiri amkuwa, ndi ngowe zasiliva ndi zingwe za mizatiyo.
[11] Mbali yakumpoto ikhalenso yotalika mamita 46 ndipo ikhale ndi nsalu
yotchinga. Pakhalenso mizati makumi awiri, matsinde amkuwa makumi
awiri, ngowe zasiliva ndi zingwe za mizatiyo.
[12] "Mbali yakumadzulo ya bwalolo ikhale yotalika mamita 23 ndipo
ikhale ndi nsalu yotchinga, nsichi khumi ndi matsinde khumi. [13] Mbali
yakummawa, kotulukira dzuwa, kutalika kwa bwalo kukhale mamita 23.
[14] Mbali imodzi yachipata kukhale nsalu yotchinga yotalika mamita asanu
ndi awiri, mizati itatu ndi matsinde atatu. [15] Ndipo ku mbali inayo kukhale
nsalu yotchinga ya mamita asanu ndi awiri pamodzi ndi mizati itatu ndi
matsinde atatu.
[16] "Pa chipata cha bwalolo pakhale nsalu yotchinga yamtundu wa
mtambo, yapepo ndi yofiira ndiponso yofewa yosalala. Nsaluyo
ikhale yotalika mamita asanu ndi anayi, yopangidwa ndi anthu aluso.
Pakhalenso mizati yake inayi ndi matsinde akenso anayi. [17] Mizati
yonse yozungulira bwalolo ilumikizidwe ndi zingwe zasiliva. Ngowe zake
zikhale zasiliva, koma matsinde ake akhale amkuwa. [18] Kutalika kwa
bwalolo kukhale mamita 46, mulifupi mwake mamita 23, msinkhu wake
masentimita 230. Nsalu ya katani ikhale yofewa ndi yosalala bwino.
Matsinde ake akhale amkuwa. [19] Zipangizo zonse zogwiritsa ntchito
zosiyanasiyana pa chihemacho, zikhomo za chihema ndi zabwalolo
zikhale zamkuwa.

### *Mafuta Anyale*

[20] "Lamula Aisraeli kuti akupatse mafuta anyale a olivi wabwino
kwambiri kuti nyalezo ziziyaka nthawi zonse. [21] M'chihema cha
msonkhano, koma kunja kwa nsalu yotchinga Bokosi la Chipangano,
Aaroni ndi ana ake azionetsetsa kuti nyale ikukhala chiyakire pamaso
pa Yehova kuyambira madzulo mpaka mmawa. Limeneli ndi lamulo
lamuyaya pakati pa Aisraeli pa mibado yonse."

## 28

### *Zovala za Ansembe*

[1] "Aaroni m'bale wako ndi ana ake aamuna, Nadabu, Abihu, Eliezara ndi
Itamara uwapatule pakati pa Aisraeli. Abwere kwa iwe kuti anditumikire

monga ansembe. 2 Umusokere m’bale wako, Aaroni, zovala zopatulika
kuti azioneka mwaulemerero ndi molemekezeka. 3 Uwawuze anthu onse
aluso amene Ine ndawapatsa nzeru pa ntchito yosoka kuti apange zovala
za Aaroni za pa mwambo womupatula, kuti iye anditumikire monga
wansembe. 4 Zovala zoti apange ndi izi: chovala chapachifuwa, efodi,
mkanjo, mwinjiro wolukidwa, nduwira ndi lamba. Apangire m’bale wako
Aaroni ndi ana ake aamuna zovala zopatulikazi kuti iwo anditumikire
monga ansembe. 5 Iwo agwiritse ntchito golide, nsalu yamtundu wa
mtambo, yapepo, yofiira ndi yosalala yofewa.

### *Efodi*

6 “Apange efodi pogwiritsa ntchito golide, nsalu yamtundu wa mtambo,
yapepo ndi yofiira yolukidwa mwaluso. 7 Efodiyo ikhale ndi timalamba
tiwiri ta pa mapewa tosokerera ku msonga zake ziwiri kuti azitha
kumanga. 8 Lamba womangira efodi akhale wolukidwa mwaluso ngati
efodiyo. Akhale wopangidwa ndi golide, nsalu yamtundu wa mtambo,
yapepo, yofiira, yofewa yosalala.
9 “Utenge miyala iwiri ya onikisi ndipo uzokotepo mayina a ana a
Israeli. 10 Mayina asanu ndi limodzi akhale pa mwala umodzi, ndipo
mayina asanu ndi limodzi pa mwala winawo motsata mabadwidwe
awo. 11 Mayina a ana a Israeli uwazokote pa miyala iwiriyo, monga
momwe amachitira mmisiri wozokota miyala. Ndipo uyike miyalayo
mu zoyikamo zake zagolide. 12 Umangirire miyala iwiriyi pa tinsalu ta
m’mapewa ta efodi tija ngati miyala ya chikumbutso cha ana a Israeli.
Aaroni azinyamula mayinawo m’mapewa ake kuti akhale chikumbutso
pamaso pa Yehova. 13 Upange zoyikamo za maluwa agolide, 14 ndiponso
maunyolo awiri a golide wabwino kwambiri, wopetedwa ngati zingwe
ndipo uwalumikize ku zoyikamozo.

### *Chovala Chapachifuwa*

15 “Upange chovala chapachifuwa chogwiritsa ntchito poweruza mlandu
ndipo uchipange mwaluso kwambiri. Uchipange ngati efodi pogwiritsa
ntchito golide, nsalu yamtundu wa mtambo, yapepo, yofiira, yofewa
yosalala ndi yolukidwa bwino. 16 Kutalika kwake kukhale kofanana
mbali zonse, mulitali masentimita 23, mulifupi masentimita 23, ndipo
chikhale chopinda pawiri. 17 Uyikepo mizere inayi ya miyala yokongola
kwambiri. Mzere woyamba ukhale ndi miyala ya rubi, topazi ndi berili.
18 Mzere wachiwiri pakhale miyala ya emeradi, safiro ndi dayimondi;
19 mzere wachitatu pakhale miyala ya opera, agate ndi ametisiti. 20 Mzere
wachinayi pakhale miyala ya topazi, onikisi ndi yasipa. Miyalayi uyiike
mu zoyikamo zagolide. 21 Miyalayo ikhalepo khumi ndi iwiri, uliwonse
kuyimira dzina limodzi la ana a Israeli. Mwala uliwonse uzokotedwe ngati
chidindo dzina limodzi la mafuko khumi ndi awiri a Israeli.
22 “Upange timaunyolo tagolide wabwino kwambiri ta pa chovala
chapachifuwa, topota ngati chingwe. 23 Upangenso mphete ziwiri zagolide
ndipo uzimangirire pa ngodya ziwiri za pa chovala chapachifuwa.
24 Umangirire timaunyolo tiwiri tagolide tija pa mphete za pa ngodya pa
chovala chapachifuwacho. 25 Ndipo mbali ina ya timaunyoloto umangirire
pa zoyikapo zake ziwiri zija ndi kulumikiza pa tinsalu takutsogolo kwa
mapewa a efodi. 26 Upangenso mphete ziwiri zagolide, ndipo uzilumikize
ku ngodya ziwiri zam’munsi mwa chovala chapachifuwa, champhepete

mwake, m'kati pafupi ndi efodi ija. 27 Upangenso mphete zina ziwiri
zagolide ndipo uzilumikize kumunsi kwa tinsalu takutsogolo kwa efodi,
pafupi ndi msoko, pamwamba pang'ono pa lamba wam'chiwuno wa efodi.
28 Tsono umangirire mphete za pa chovala chapachifuwa zija ku mphete za
efodi ndi chingwe chamtundu wa mtambo, kulumikiza lamba ndi chovala
chapachifuwacho kuti chovala chapachifuwacho chisalekane ndi efodi.
29 "Pamene Aaroni akulowa kumalo opatulika azivala chovala cha-
pachifuwa cha zoweruzira chija chimene chalembedwa mayina a ana a
Israeli kuti Yehova awakumbukire nthawi zonse. 30 Ndiponso uyike Urimu
ndi Tumimu mu chovala chapachifuwa cha zoweruziracho, kuti zikhale
pamtima pa Aaroni. Choncho Aaroniyo adzakhala akutenga nthawi zonse
zida zomuthandizira kuweruza ana a Israeli pamene adzafika pamaso pa
Yehova.

*Zovala Zina za Ansembe*

31 "Uyipangire efodiyo mkanjo wamtundu wa mtambo. 32 Mkanjowo
ukhala ndi malo opisapo mutu pakati pakepo. Pa chibowopo pakhale
chibandi chosokedwa mochita ngati kuluka monga muja akhalira malaya
kuti chibowocho chilimbe, chisang'ambike. 33 Pa mpendero wam'munsi
wa mkanjowo, upange mphonje zokhala ngati makangadza za nsalu
yamtundu wa mtambo, yapepo ndi yofiira zokhala ndi maberu agolide
pakati pake. 34 Choncho pazikhala mphonje imodzi kenaka belu limodzi,
kuzungulira mpendero wa mkanjo wonse. 35 Aaroni azivala mkanjowo
pamene akutumikira ngati wansembe. Kulira kwa maberu kuzimveka
pamene akulowa m'malo opatulika pamaso pa Yehova ndiponso pamene
akutuluka, kuti asafe.
36 "Upange duwa lagolide wabwino kwambiri kukhala ngati chidindo
ndipo uzokotepo mawu akuti, COHOPEREKEDWA KWA YEHOVA. 37 Ulimange
ndi chingwe cha nsalu yamtundu wa mtambo pa nduwira ya Aaroni,
ndipo duwalo likhale kutsogolo kwa nduwirayo. 38 Lidzakhala pa
mphumi ya Aaroni, motero iye adzasenza cholakwa chilichonse cha pa
zopereka zilizonse zimene Aisraeli amazipatulira Yehova. Aaroni azivala
chikwangwanichi pa mphumi pake nthawi zonse kuti Yehova alandire
zopereka za anthu ake.
39 "Uluke mwinjiro wa nsalu yofewa yosalala ndiponso upange nduwira
ya nsalu yofewa yosalala. Lamba wake akhale wolukidwa bwino ndi
munthu waluso. 40 Upangirenso ana a Aaroni mwinjiro, malamba ndi
nduwira kuti azioneka mwaulemu ndi molemekezeka. 41 Zovala zimenezi
umuveke Aaroni, m'bale wako ndi ana ake. Kenaka uwadzoze, uwapatse
udindo ndi kuwapatula kuti anditumikire ngati ansembe anga.
42 "Uwapangire akabudula a nsalu yofewa oyambira m'chiwuno
kulekeza m'ntchafu kuti asamaonetse maliseche. 43 Aaroni ndi ana ake
ayenera kuvala akabudulawo pamene akulowa mu tenti ya msonkhano
kapena pamene akupita ku guwa lansembe kukatumikira malo oyera
kuopa kuti angachimwe ndi kufa.
"Ili likhale lamulo la nthawi zonse kwa Aaroni ndi zidzukulu zake."

# 29

*Mwambo Wopatula Ansembe*

1 "Pofuna kumupatula Aaroni ndi ana ake kuti akhale ansembe
onditumikira Ine, uchite izi: Utenge ng'ombe yaying'ono yayimuna ndi

nkhosa ziwiri zazimuna zopanda chilema. 2 Utengenso buledi wopanda
yisiti, makeke wopanda yisiti wopakidwa mafuta. Zonsezi uzipange ndi
ufa wosalala wa tirigu. 3 Uziyike m'dengu ndipo ubwere nazo kwa Ine
pamodzi ndi ng'ombe yayimuna ija ndi nkhosa ziwiri zazimuna zija.
4 Kenaka ubwere naye Aaroni ndi ana ake pa khomo la tenti ya msonkhano
ndipo uwasambitse ndi madzi. 5 Tenga zovala ndipo umuveke Aaroni
mwinjiro, mkanjo wa efodi, efodiyo ndi chovala chapachifuwa. Umu-
mange m'chiwuno lamba wa efodi wolukidwa mwaluso uja. 6 Umuveke
nduwira kumutu, ndiponso uyike chizindikiro chopatulika chija pa
nduwirayo. 7 Utenge mafuta wodzozera ndipo uwatsanulire pamutu pake
kumudzoza. 8 Ubwere ndi ana ake aamuna ndipo uwavekenso minjiro
9 ndi nduwira. Kenaka umange malamba Aaroniyo pamodzi ndi ana ake
ndi kuwaveka nduwira. Motero unsembe udzakhala wawo malingana ndi
lamulo ili losatha.

"Umu ndi mmene udzadzozere Aaroni ndi ana ake aamuna.

10 "Ubwere ndi ng'ombe yayimuna pa khomo la tenti ya msonkhano
ndipo Aaroni ndi ana ake asanjike manja awo pamutu pake. 11 Uphe
ng'ombeyo pamaso pa Yehova pa khomo la tenti ya msonkhano. 12 Utenge
magazi ena ang'ombeyo ndi kupaka ndi chala chako pa nyanga zaguwa
lansembe ndipo magazi otsalawo uwakhutulire pa tsinde laguwalo.
13 Kenaka utenge mafuta onse okuta matumbo, mafuta ophimba chiwindi
ndiponso impsyo zonse ziwiri pamodzi ndi mafuta ake. Zonsezi uzitenthe
pa guwapo. 14 Koma nyama yang'ombeyo, chikopa chake ndi matumbo
ake uziwotche kunja kwa msasa. Iyi ndi nsembe yopepesera machimo.

15 "Utenge nkhosa yayimuna imodzi ndipo Aaroni ndi ana ake aamuna
asanjike manja awo pamutu pake. 16 Uyiphe ndipo utenge magazi ake
ndi kuwaza mbali zonse zaguwalo. 17 Uyidule nkhosayo nthulinthuli,
kutsuka matumbo ake ndi miyendo yake. Ukatero, pamodzi ndi mutu
wake, uziyike pamwamba pa nthulizo. 18 Ndipo uwotche nkhosa yonseyo
pa guwa lansembe. Iyi ndi nsembe yopsereza ya kwa Yehova. Ili ndi fungo
lokoma, loperekedwa pa moto kwa Yehova.

19 "Utenge nkhosa yayimuna ina ndipo Aaroni ndi ana ake aamuna
asanjike manja awo pamutu pake. 20 Uyiphe ndipo utenge magazi ake ena
ndi kupaka ndewere za makutu a kudzanja lamanja la Aaroni ndi ana ake
aamuna. Upakenso pa zala zawo zazikulu za kudzanja lawo lamanja, ndi
zala zazikulu za kuphazi lakudzanja lawo lamanja. Kenaka uwaze magazi
otsalawo mbali zonse za guwalo. 21 Ndipo utenge magazi ena amene ali
pa guwa lansembe komanso pa mafuta ena odzozera ndipo uwawaze pa
Aaroni ndi zovala zake ndi ana ake ndi zovala zawo. Ndiye kuti iyeyo ndi
ana ake aamuna adzakhala opatulika pamodzi ndi zovala zawo.

22 "Pa nkhosa yayimuna ija utengepo mafuta ake, mafuta a ku mchira
wake, mafuta okuta matumbo, mafuta okuta chiwindi, impsyo zonse ziwiri
ndi mafuta ake, ndiponso ntchafu yakumanja. Iyi ndi nkhosa ya mwambo
wodzoza. 23 Utengenso m'dengu la buledi wopanda yisiti limene lili
pamaso pa Yehova, buledi mmodzi, buledi wokhala ndi mafuta a olivi,
ndi buledi wopyapyala mmodzi. 24 Izi zonse uzipereke m'manja mwa
Aaroni ndi ana ake, ndipo iwo aziweyule pamaso pa Yehova kuti zikhale
nsembe yoweyula. 25 Kenaka uzitenge m'manja mwawo ndipo uzipsereze
pa guwa lansembe, pamwamba penipeni pamodzi ndi nsembe yopsereza
kuti ipereke fungo lokoma kwa Yehova. Ichi ndiye chopereka chachakudya

kwa Yehova. 26 Kenaka utenge chidale cha nkhosa yayimuna imene
inaperekedwa pamwambo wodzoza Aaroni, uchiweyule kuti chikhale
nsembe yoweyula pamaso pa Yehova ndipo chidzakhala gawo lako.

27 "Uzipatule ziwalo zonse za nkhosa ya pa mwambo wodzoza Aaroni
ndi ana ake. Chidale chimene unaweyula chija ndiponso ntchafu imene
inaperekedwa ija. 28 Nsembe izi ndi zimene Aisraeli azipereka kwa Aaroni
ndi ana ake mwa zonse zimene azipereka nthawi zonse. Mwa zopereka za
mtendere zimene ana a Aisraeli adzapereka kwa Yehova, zimenezi zikhale
gawo lawo.

29 "Zovala zopatulika za Aaroni zidzakhala za ana ake aamuna iye
atafa kuti adzavale podzozedwa ndi polandira udindo wawo. 30 Mwana
amene adzalowa m'malo mwake monga wansembe pamene adzabwerera
kudzalowa mu tenti ya msonkhano kudzatumikira ku malo wopatulika,
adzavala zovala zimenezi masiku asanu ndi awiri.

31 "Utenge nkhosa yayimuna ya pamwambo wodzoza ansembe ndipo
uyiphike pamalo opatulika. 32 Aaroni ndi ana ake adye nyama ya
nkhosa yayimunayi pamodzi ndi buledi amene ali m'dengu pa khomo
la tenti ya msonkhano. 33 Adye zonse zimene anazipereka kwa Yehova
pamwambo wopepesera machimo powadzoza ndi kuwapatula. Munthu
wamba asadye chifukwa ndi zopatulika. 34 Ndipo ngati nyama ina ya
nkhosa ya pamwambo wodzoza ansembe kapena buledi zatsala mpaka
mmawa, muziwotche, asazidye chifukwa ndi zopatulika.

35 "Uchitire Aaroni ndi ana ake aamuna zonse zimene ndakulamulazi.
Uchite mwambo wowapatula kukhala ansembe masiku asanu ndi awiri.
36 Tsiku lililonse uzipereka ng'ombe yayimuna ngati nsembe yopepesera
machimo kuti machimowo akhululukidwe. Ndiponso upatule guwalo
popereka nsembe yopepesera ndi kulidzoza mafuta kuti likhale lopatulika.
37 Pa masiku asanu ndi awiri uzipereka pa guwapo nsembe zoyeretsera
guwalo, ukatero ndiye kuti uzilipatula. Ndipo guwa lansembelo lidzakhala
loyera kwambiri, ndipo chilichonse chimene chidzakhudza guwalo chidza-
yeretsedwa.

38 "Tsiku ndi tsiku pa guwa lansembe uzipereka izi: Ana ankhosa
a chaka chimodzi awiri. 39 Mmawa muzipereka mwana wankhosa
mmodzi ndipo winayo madzulo. 40 Pamodzi ndi mwana wankhosa
woyambayo, muzipereka kilogalamu imodzi ya ufa wosalala wosakaniza
ndi lita imodzi ya mafuta a olivi pamodzi ndi lita imodzi ya vinyo ngati
chopereka chachakumwa. 41 Upereke mwana wankhosa winayo madzulo
pamodzi ndi chopereka chachakudya monga poyamba paja ndi chopereka
chachakumwa monga mmawa kuti ikhale fungo lokoma la chopereka
chachakudya kwa Yehova.

42 "Zopereka zopsereza zimenezi ziziperekedwa nthawi zonse, pa
mibado yonse. Muzidzazipereka pamaso pa Yehova pa khomo la tenti
ya msonkhano. Pa guwa lansembe, Yehova adzakumana nanu ndi
kuyankhula nanu. 43 Pameneponso Ine ndidzakumana ndi Aisraeli, ndipo
guwalo lidzakhala lopatulika chifukwa cha ulemerero wanga.

44 "Tsono Ine ndidzapatula tenti ya msonkhano ndi guwa lansembe.
Ndidzapatulanso Aaroni pamodzi ndi ana ake kuti akhale ansembe anga
onditumikira. 45 Ndidzakhala pakati pa Aisraeli ndikukhala Mulungu
wawo. 46 Adzadziwa kuti ine ndine Mulungu wawo amene ndinawatulutsa
m'dziko la Igupto kuti ndikhale pakati pawo. Ine ndine Yehova, Mulungu
wawo."

# 30

### *Guwa Lansembe Yofukiza*

1 Upange guwa lamatabwa amtengo wa mkesha lofukizirapo lubani.
2 Likhale lofanana mbali zonse. Mulitali masentimita 46, mulifupi
masentimita 46, ndipo msinkhu masentimita 91. Nyanga zake zipangidwe
kumodzi ndi guwalo. 3 Ukute guwa lonse ndi golide wabwino kwambiri,
pamwamba pake, mbali zonse zinayi, pamodzi ndi nyanga zake. Ndipo
upange mkombero wagolide kuzungulira guwalo. 4 Upange mphete ziwiri
zagolide ndipo uzilumikize ku guwa m'munsi mwa mkombero, mphete
ziwiri ku mbali zonse ziwiri zoyang'anana. Mphetozo zizigwira nsichi
zonyamulira guwalo. 5 Upange mizati yamtengo wa mkesha ndipo uyikute
ndi golide. 6 Uyike guwalo patsogolo pa nsalu yotchinga Bokosi la
Chipangano. Apa ndi pamene ndizidzakumana nawe.
7 "Aaroni ayenera kumafukiza lubani wonunkhira pa guwalo mmawa
uliwonse. Pamene akukonza nyale zija afukizenso lubani. 8 Aaroni ayen-
era kufukizanso lubani pamene ayatsa nyale madzulo kuti lubani akhale
akuyaka nthawi zonse pamaso pa Yehova kwa mibado imene ikubwera.
9 Pa guwapo usafukize lubani wachilendo kapena kuperekapo nsembe
yopsereza kapena nsembe yaufa. Usathire pa guwapo ngakhale nsembe
yachakumwa. 10 Aaroni azidzapereka nsembe yopepesera machimo
pa nyanga za guwalo kamodzi pa chaka. Mwambowu uzidzachitika
pogwiritsa ntchito magazi a nsembe yopepesera machimo, ndipo zizidza-
chitika m'mibado yanu yonse. Choncho guwa lansembelo lidzakhala
loyera ndi loperekedwa kwa Yehova."

### *Za Chopereka Chowombolera Moyo*

11 Ndipo Yehova anati kwa Mose, 12 "Pamene ukuchita kalembera wa
Aisraeli, munthu aliyense ayenera kupereka kwa Yehova chowombolera
moyo wake pamene akuwerengedwa. Motero mliri sudzabwera pa iwo
pamene ukuwawerenga. 13 Izi ndi zimene aliyense wolembedwa mu
kawundula ayenera kupereka: theka la sekeli, kutanthauza ndalama
zolemera magalamu asanu ndi limodzi malingana ndi kawerengedwe
ka ndalama za ku Nyumba ya Mulungu. Paja sekeli imodzi ikulingana
ndi magera makumi awiri. Theka la sekeli chidzakhala chopereka cha
kwa Yehova. 14 Aliyense wolembedwa mu kawundula amene ali ndi
zaka makumi awiri kapena kupitirira ayenera kupereka chopereka kwa
Yehova. 15 Anthu olemera asapereke koposa theka la sekeli ndipo osauka
asapereke kuchepera theka la sekeli pamene mukupereka nsembe kwa
Yehova yowombolera miyoyo yanu. 16 Ulandire ndalama zopepeserazo
kuchokera kwa Aisraeli ndipo zigwiritsidwe ntchito ya ku tenti ya
msonkhano. Zoperekazi zidzakhala chikumbutso cha Aisraeli pamaso pa
Yehova, ndiponso zowombolera miyoyo yanu."

### *Za Beseni Losambira*

17 Ndipo Yehova anati kwa Mose, 18 "Upange beseni lamkuwa lokhala
ndi miyendo yamkuwanso. Uliyike pakati pa tenti ya msonkhano ndi guwa
lansembe ndipo uthiremo madzi. 19 Aaroni ndi ana ake azisamba m'manja
ndi kutsuka mapazi awo ndi madzi amenewo. 20 Pamene akulowa mu
tenti ya msonkhano, iwo asambe madziwa kuti asafe. Ndiponso pamene
akupita kukatumikira ku guwa lansembe ndi kupereka nsembe yopsereza
kwa Yehova, 21 azisamba m'manja mwawo ndi kutsuka mapazi kuti

asadzafe. Limeneli ndi lamulo limene Aaroni, pamodzi ndi ana ndi zidzukulu zake m'tsogolomo ayenera kumadzalitsatira mpaka muyaya."

### *Mafuta Wodzozera*

22 Ndipo Yehova anati kwa Mose, 23 "Utenge zonunkhira bwino kwambiri
izi: makilogalamu asanu ndi limodzi a mure wamadzi, makilogalamu
atatu a zonunkhira bwino za mtundu wa sinamoni, makilogalamu atatu a
nzimbe yonunkhira bwino kwambiri, 24 makilogalamu asanu ndi limodzi
a mkesha. Zonsezi zikhale malingana ndi muyeso wa ku Nyumba ya
Mulungu. Pakhalenso malita anayi a mafuta a olivi. 25 Ugwiritse ntchito
zinthu zimenezi kupanga mafuta opatulika odzozera, mafuta onunkhira,
apangidwe ndi m'misiri waluso lopanga zonunkhiritsa. Awa adzakhala
mafuta opatulika odzozera. 26 Tsono uwagwiritse ntchito podzoza tenti
ya msonkhano, Bokosi la Chipangano, 27 tebulo, ndi ziwiya zake zonse,
choyikapo nyale ndi zipangizo zake, guwa lofukizirapo lubani, 28 guwa
lansembe yopsereza ndi ziwiya zake zonse, ndiponso beseni pamodzi
ndi nsichi yake. 29 Zonsezi uzipatule kuti zidzakhale zopatulika, ndipo
chilichonse chimene chidzakhudza zimenezi chidzakhala chopatulika.
30 "Udzoze Aaroni ndi ana ake aamuna ndi kuwapatula kuti akhale
ansembe onditumikira. 31 Tsono awuze a Israeli kuti, mafuta wodzozera
awa adzakhala wopatulika mpaka muyaya. 32 Musadzadzozere munthu
wamba mafuta amenewa, ndipo musadzapange mafuta wofanana ndi
amenewa. Mafutawa ndi wopatulika ndipo akhale woyera kwa inu.
33 Wina aliyense amene adzapanga mafuta wonunkhira wofanana nawo
kapena kudzozera mafutawa munthu wamba osati wansembe ayenera
kuchotsedwa pakati pa anthu anzake."

### *Za Zofukiza*

34 Kenaka Yehova anati kwa Mose, "Tenga muyeso wofanana wa zinthu
zonunkhira izi: sitakate, onika, galibanumu pamodzi ndi lubani weniweni.
35 Uziphatikize pamodzi zonsezi ndi kupanga lubani monga amachitira
mmisiri wopanga zonunkhira. Athire mchere ndipo akhale woyera
ndi wopatulika. 36 Upere gawo lina mosalala kwambiri ndipo utapepo
pang'ono ndi kuyika patsogolo pa Bokosi la Chipangano mu tenti ya
msonkhano, kumene ine ndidzakumane nawe. Lubani ameneyu kwa inu
adzakhala wopatulika kwambiri. 37 Musapange lubani wanu potsatira
njira iyi. Lubani yense wopangidwa mwa njira iyi akhale wopatulika,
woperekedwa kwa Yehova. 38 Aliyense amene adzapanga wofanana naye
kuti asangalale ndi fungo lake ayenera kuchotsedwa pakati pa anthu
anzake."

## 31

### *Bezaleli ndi Oholiabu*

1 Ndipo Yehova anati kwa Mose, 2 "Taona, ndasankha Bezaleli mwana
wa Uri, mwana wa Huri, wa fuko la Yuda. 3 Ndipo ndamudzaza ndi
Mzimu wa Mulungu kotero kuti ali ndi luso ndi nzeru zomvetsa zinthu
ndipo akudziwa bwino ntchito zonse zamanja monga izi: 4 Kulemba
ndondomeko ya ntchito zaluso ndi kupanga zinthu zagolide, zasiliva ndi
zamkuwa, 5 kusema ndi kuyika miyala yokongola, kukonza zinthu za-
matabwa ndiponso kugwira ntchito ina iliyonse yamanja. 6 Ndasankhanso
Oholiabu mwana wa Ahisamaki wa fuko la Dani. Ndiponso ndapereka

nzeru kwa anthu aluso motero adzagwira ntchito zonse zimene ndaku-
lamulira kuti zichitike monga izi: 7 Kupanga tenti ya msonkhano, bokosi
laumboni pamodzi ndi chophimbira chake, ndiponso zonse za mu tenti,
8 tebulo ndi zida zake, choyikapo nyale cha golide wabwino kwambiri ndi
ziwiya zake zonse, guwa lofukizirapo lubani, 9 guwa lansembe yopsereza
ndi ziwiya zake zonse, beseni ndi nsichi yake, 10 ndiponso zovala zonse
zolukidwa, zovala zopatulika za Aaroni wansembe pamodzi ndi za ana
ake, zovala pamene akutumikira monga ansembe, 11 ndiponso mafuta
odzozera ndi lubani wonunkhira wa ku malo opatulika. Iwo azipanga
monga momwe Ine ndinakulamulira."

### *Za Sabata*

12 Ndipo Yehova anati kwa Mose, 13 "Uza ana a Israeli kuti azisunga
Masabata anga. Ichi chidzakhala chizindikiro pakati pa inu ndi Ine
pamodzi ndi zidzukulu zanu m'tsogolomo, chosonyeza kuti Ine ndine
amene ndimakuyeretsani.

14 "Motero muzisunga tsiku la Sabata chifukwa ndi loyera kwa inu.
Aliyense amene adetsa tsiku la Sabata ayenera kuphedwa. Aliyense
amene agwira ntchito iliyonse pa tsikuli ayenera kuchotsedwa pakati
pa anthu anzake. 15 Mugwire ntchito kwa masiku asanu ndi limodzi
koma tsiku lachisanu ndi chiwiri ndi Sabata, lopuma, tsiku lopatulika
la Yehova. Aliyense amene agwira ntchito iliyonse pa tsiku la Sabata
ayenera kuphedwa. 16 Aisraeli onse komanso zidzukulu zawo m'tsogolo
azidzasunga tsiku la Sabata ngati pangano lamuyaya. 17 Tsiku la Sabata
lidzakhala chizindikiro chamuyaya pakati pa Ine ndi Aisraeli chosonyeza
kuti Yehova analenga za kumwamba ndi dziko lapansi kwa masiku asanu
ndi limodzi ndi kuti pa tsiku lachisanu ndi chiwiri analeka kugwira ntchito
napumula."

18 Yehova atamaliza kuyankhula ndi Mose pa phiri la Sinai, anamupatsa
Mose miyala iwiri yaumboni, imene Mulungu analembapo ndi chala
chake.

# 32

### *Za Fano la Mwana Wang'ombe Wagolide*

1 Anthu ataona kuti Mose akuchedwa kutsika m'phiri, anasonkhana
kwa Aaroni ndipo anati, "Bwera utipangire milungu imene idzititsogolera.
Kunena za Mose amene anatitulutsa m'dziko la Igupto, sitikudziwa
chimene chamuchitikira."

2 Aaroni anawayankha kuti, "Vulani ndolo zagolide zimene avala
akazi anu, ana anu aamuna ndi aakazi ndipo muzibweretse kwa ine."
3 Kotero anthu onse anavula ndolo zagolide ndi kubwera nazo kwa
Aaroni. 4 Choncho Aaroni analandira golideyo ndipo anamuwumba ndi
chikombole ndi kupanga fano la mwana wang'ombe. Kenaka anthu aja
anati, "Inu Aisraeli, nayu mulungu wanu amene anakutulutsani m'dziko
la Igupto."

5 Aaroni ataona izi, anamanga guwa lansembe patsogolo pa mwana
wang'ombeyo ndipo analengeza kuti, "Mawa kudzakhala chikondwerero
cha Yehova." 6 Kotero tsiku linalo anthu anadzuka mmamawa ndithu ndi
kupereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano. Atatha kupereka
nsembezo, anthuwo anakhala pansi nayamba kudya ndi kumwa. Kenaka
anayimirira nayamba kuvina mwachilendo.

7 Pamenepo Yehova anati kwa Mose, “Tsika msanga, chifukwa anthu ako
amene unawatulutsa m’dziko la Igupto aja adziyipitsa kwambiri. 8 Iwo
apatuka mwamsanga kuleka kutsatira zimene ndinawalamula. Ndiye
adzipangira fano la mwana wang’ombe. Aligwadira ndi kuliperekera
nsembe n’kumati, ‘Inu Aisraeli, nayu mulungu wanu amene anakutulut-
sani m’dziko la Igupto.’ ”
9 Yehova anati kwa Mose, “Ine ndikuwadziwa anthu amenewa. Iwowa
ndi ankhutukumve. 10 Chifukwa chake undileke kuti mkwiyo wanga
uyake pa iwo ndi kuwawononga. Ndipo Ine ndidzakusandutsa kuti ukhale
mtundu waukulu.”
11 Koma Mose anapempha chifundo cha Mulungu wake ndipo anati,
“Chonde Yehova, chifukwa chiyani mwakwiyira anthu awa amene
munawatulutsa m’dziko la Igupto ndi mphamvu yanu yayikulu ndi
dzanja lanu lamphamvu. 12 Kodi mukufuna kuti Aigupto azinena kuti,
‘Munali ndi cholinga choyipa chofuna kuwaphera ku mapiri kuno ndi
kuwawonongeratu pa dziko lapansi pamene munkawatulutsa ku Igupto
kuja?’ Ayi, chonde mkwiyo wanu woyaka ngati motowu ubwezeni ndipo
sinthani maganizo ofunira zoyipa anthu anu. 13 Kumbukirani atumiki anu,
Abrahamu, Isake, Israeli ndi zija munawalonjeza polumbira pa dzina lanu
kuti, ‘Ine ndidzachulukitsa zidzukulu zanu ndipo zidzakhala zambiri ngati
nyenyezi zakumwamba. Zidzukulu zanuzo ndidzazipatsa dziko lonseli
limene ndinalonjeza. Dziko limeneli lidzakhala lawo nthawi zonse.’ ”
14 Choncho Yehova analeka ndipo sanawachitire choyipa anthu ake monga
anaopsezera.
15 Mose anatembenuka ndi kutsika phiri miyala iwiri ya pangano ili
m’manja mwake. Miyalayi inalembedwa mbali zonse, kutsogolo ndi
kumbuyo komwe. 16 Miyalayi anayikonza ndi Mulungu. Malembawo
analemba ndi Mulungu mozokota pa miyalapo.
17 Pamene Yoswa anamva phokoso la anthu anati kwa Mose, “Ku msasa
kuli phokoso la nkhondo.”
18 Mose anayankha kuti,
“Phokoso limeneli sindikulimva
ngati phokoso la opambana nkhondo,
kapena kulira kwa ongonjetsedwa pa nkhondo. Koma ndikulimva
ngati phokoso la anthu amene akuyimba.”
19 Mose atayandikira msasa ndi kuona mwana wang’ombe ndiponso
kuvina, anakwiya kwambiri ndipo anaponya pansi miyala imene inali
m’manja mwake, ndi kuyiphwanya pa tsinde la phiri. 20 Ndipo iye
anatenga mwana wang’ombe amene anthu anapanga uja ndi kumuwotcha
pa moto ndi kumuperapera ndikukhala ngati fumbi. Kenaka anawaza
fumbilo m’madzi ndi kuwamwetsa Aisraeli madziwo.
21 Tsono Mose anafunsa Aaroni kuti, “Kodi anthu awa anakuchita
chiyani kuti uwachimwitse koopsa chotere?”
22 Aaroni anayankha kuti, “Musakwiye mbuye wanga. Inu mukudziwa
kuti anthu awa ndi ovuta. 23 Iwo anati kwa ine, ‘Bwera utipangire
milungu imene idzititsogolera. Kunena za Mose amene anatitulutsa ife
m’dziko la Igupto, sitikudziwa chimene chamuchitikira.’ 24 Choncho
ine ndinawawuza kuti, ‘Aliyense amene ali ndi zokometsera zagolide
azivule.’ Choncho iwo anandipatsa golide, ndipo ndinamuponya pa moto
ndi kupanga fano la mwana wang’ombeyu.”
25 Mose anaona kuti anthuwo anali osokonezekadi chifukwa Aaroni
anawalekerera mpaka kusanduka anthu osekedwa pakati pa adani awo.

26 Choncho iye anayima pa chipata cholowera mu msasa ndipo anati,
“Aliyense amene ali mbali ya Yehova abwere kwa ine.” Ndipo Alevi onse
anapita mbali yake.
27 Ndipo iye anawawuza kuti, “Izi ndi zimene Yehova Mulungu wa
Israeli akunena, ‘Pitani ku misasa konse, mulowe ku zipata zonse ndipo
aliyense akaphe m’bale wake, kapena mnzake kapena mnansi wake.’ ”
28 Alevi anachita zomwe Mose analamula, ndipo tsiku limenelo panafa
anthu pafupifupi 3,000. 29 Kenaka Mose anati, “Lero mwadzipatula
nokha kukhala ansembe otumikira Yehova. Mwachita izi popeza aliyense
wa inu wapha mwana wake kapena m’bale wake. Tsono lero Yehova
wakudalitsani.”
30 Mmawa mwake Mose anati kwa anthu onse, “Inu mwachita tchimo
lalikulu. Koma tsopano ine ndipita ku phiri kwa Yehova mwina ndikatha
kukupepeserani chifukwa cha tchimo lanu.”
31 Kotero Mose anabwereranso kwa Yehova ndipo anati, “Aa! Anthu
awa achita tchimo lalikulu! Iwo adzipangira milungu yagolide. 32 Koma
tsopano, chonde akhululukireni tchimo lawo. Ngati simutero, ndiye
mundifute ine m’buku limene mwalemba.”
33 Yehova anamuyankha Mose kuti, “Ndidzafuta m’buku aliyense amene
wandichimwira. 34 Tsopano pita ukawatsogolere anthu kumalo kumene
ine ndinanena, ndipo mngelo wanga adzakutsogolerani. Komabe, nthawi
yanga ikadzafika kuti ndiwalange, ndidzawalanga chifukwa cha tchimo
lawo.”
35 Ndipo Yehova anawakantha anthuwo ndi mliri chifukwa anawumi-
riza Aaroni kuti awapangire fano la mwana wang’ombe.

# 33

1 Ndipo Yehova anati, “Chokani pa malo ano, iwe ndi anthu amene
unawatulutsa m’dziko la Igupto. Pitani ku dziko limene ine ndinalonjeza
ndi lumbiro kwa Abrahamu, Isake ndi Yakobo kuti, ‘Ine ndidzalipereka
kwa zidzukulu zanu.’ 2 Ndipo ndidzatumiza mngelo patsogolo panu
kuthamangitsa Akanaani, Aamori, Ahiti, Aperezi, Ahivi ndi Ayebusi.
3 Pitani ku dziko loyenda mkaka ndi uchi. Koma ine sindidzapita nanu,
chifukwa anthu inu ndinu nkhutukumve ndipo nditha kukuwonongani
m’njiramo.”
4 Anthu atamva mawu owopsawa, anayamba kulira ndipo palibe
anavala zodzikometsera. 5 Pakuti Yehova anali atanena kwa Mose kuti,
“Awuze Aisraeli kuti, ‘Inu ndinu nkhutukumve.’ Ngati ine ndipita ndi inu
kwa kanthawi, nditha kukuwonongani. Tsopano vulani zodzikometsera
zanu ndipo ine ndidzaganiza choti ndichite nanu.” 6 Kotero Aisraeli
anavula zodzikometsera zawo pa phiri la Horebu.

### *Tenti ya Msonkhano*

7 Tsono Mose ankatenga tenti ndi kukayimanga kunja kwa msasa
chapatalipo, ndipo ankayitcha “tenti ya msonkhano.” Aliyense wofuna
kukafunsa kanthu kwa Yehova amapita ku tenti ya msonkhano kunja
kwa msasa. 8 Ndipo nthawi ina iliyonse imene Mose amapita ku tenti
anthu onse amanyamuka ndi kuyimirira pa makomo amatenti awo,
kumuyang’ana Mose mpaka atalowa mu tentimo. 9 Mose akamalowa mu
tenti, chipilala cha mtambo chimatsika ndi kukhala pa khomo pamene
Yehova amayankhula ndi Mose. 10 Nthawi zonse anthu akaona chipilala
cha mtambo chitayima pa khomo la tentiyo amayimirira ndi kupembedza,

aliyense ali pa khomo la tenti yake. 11 Yehova amayankhula ndi Mose maso
ndi maso ngati mmene munthu amayankhulira ndi bwenzi lake. Kenaka
Mose amabwerera ku msasa koma womuthandiza wake, Yoswa, mwana
wa Nuni samachoka pa tentiyo.

*Mose ndi Ulemerero wa Yehova*

12 Mose anati kwa Yehova, "Inu mwakhala mukundiwuza kuti, 'Tsogol-
era anthu awa,' koma simunandiwuze amene mudzamutuma kuti apite
pamodzi nane. Inu mwanena kuti, 'Ndikukudziwa bwino kwambiri ndipo
wapeza chisomo pamaso panga.' 13 Ngati mwakondwera nane ndiphunz-
itseni njira zanu kuti ndikudziweni ndi kupitiriza kupeza chisomo pamaso
panu. Kumbukirani kuti mtundu uwu ndi anthu anu."

14 Yehova anayankha kuti, "Ine ndemwe ndidzapita pamodzi ndi iwe,
ndipo ndidzakupatsa mpumulo."

15 Kenaka Mose anati kwa Yehova, "Ngati inu simupita nafe, musatitu-
mize kuti tipite, kutichotsa pano. 16 Kodi wina adzadziwa bwanji kuti inu
mwandikomera mtima pamodzi ndi anthu awa ngati simupita nafe? Kodi
n'chiyani chomwe chidzatisiyanitse pakati pa anthu onse amene ali pa
dziko lapansi?"

17 Ndipo Yehova anati kwa Mose, "Ine ndidzachita zimene iwe
wandipempha chifukwa Ine ndikukondwera nawe, ndikukudziwa bwino
lomwe."

18 Kenaka Mose anati, "Tsopano ndionetseni ulemerero wanu."

19 Ndipo Yehova anati, "Ine ndidzakuonetsa ulemerero wanga wonse
ndipo ndidzatchula dzina langa lakuti Yehova pamaso pako. Ine
ndidzachitira chifundo amene ndikufuna kumuchitira chifundo ndipo
ndidzakomera mtima amene ndikufuna kumukomera mtima." 20 Iye anati,
"Koma iwe sungaone nkhope yanga, pakuti palibe munthu amene amaona
Ine nakhala ndi moyo."

21 Ndipo Yehova anati, "Pali malo pafupi ndi ine pomwe ungathe
kuyima pa thanthwe. 22 Pamene ulemerero wanga udutsa, ndidzakuyika
m'phanga la thanthwe ndi kukuphimba ndi dzanja langa mpaka ndi-
tadutsa. 23 Kenaka ine ndidzachotsa dzanja langa ndipo iwe udzaona
msana wanga, koma nkhope yanga sidzaoneka."

# 34

*Miyala ina Yatsopano*

1 Yehova anati kwa Mose, "Sema miyala iwiri yofanana ndi yoyamba
ija, ndipo Ine ndidzalembapo mawu amene anali pa miyala yoyamba ija,
imene unayiphwanya. 2 Ukonzeke mmamawa, ndipo ubwere ku Phiri la
Sinai. Udzaonekera pamaso panga pamwamba pa phiri. 3 Palibe amene
abwere nawe kapena kuoneka pena paliponse pafupi ndi phiri. Ndipo
ngakhale nkhosa kapena ng'ombe zisadye m'mbali mwa phirilo."

4 Choncho Mose anasema miyala iwiri yofanana ndi yoyamba ija ndipo
anapita ku Phiri la Sinai mmawa atanyamula miyala iwiri m'manja
mwake monga momwe Yehova anamulamulira. 5 Ndipo Yehova anatsika
mu mtambo ndi kuyima pamodzi ndi Mose ndi kulengeza dzina lake
lakuti Yehova. 6 Ndipo Iye anadutsa kutsogolo kwa Mose akulengeza
kuti, "Yehova, Yehova, Mulungu wachifundo ndi wokoma mtima, wosapsa
mtima msanga, wodzaza ndi chikondi chosasinthika ndi kukhulupirika,

7 waonetsa chikondi chosasinthika kwa anthu miyandamiyanda, wokhul-
ulukira zoyipa, kuwukira, ndiponso tchimo, komatu salekerera ochimwa
kuti asalangidwe. Iye amalanga ana ndi zidzukulu chifukwa cha machimo
a makolo awo mpaka m'bado wachitatu ndi wachinayi."

8 Pamenepo Mose anawerama pansi napembedza. 9 Iye anati, "Chonde
Ambuye, ngati ndapeza chisomo pamaso panu, lolani Ambuye kuti mupite
nafe pamodzi. Ngakhale kuti anthuwa ndi nkhutukumve, khululukirani
zoyipa ndi machimo athu, ndipo mutenge ife kukhala anthu anu."

10 Choncho Yehova anati: "Ine ndikuchita nanu pangano. Ndidzachita
zodabwitsa pamaso pa anthu onse zimene sizinachitikenso ndi mtundu
wina uliwonse wa anthu pa dziko lonse lapansi. Anthu amene mudzakhala
pakati pawo adzaona kuopsa kwa ntchito imene Ine Yehova ndidzakuchi-
tireni. 11 Mverani zimene ndikukulamulirani lero. Ine ndidzathamangitsa
pamaso panu Aamori, Akanaani, Ahiti, Aperezi, Ahivi, ndi Ayebusi.
12 Musamale kuti musakachite mgwirizano ndi anthu amene akukhala
m'dziko limene mukupitalo, chifukwa mukadzatero iwo adzakhala ngati
msampha pakati panu. 13 Mukagumule maguwa awo ansembe, mukaswe
miyala yawo yachipembedzo, ndipo mukadule mitengo yawo ya Asera.
14 Musapembedze mulungu wina, pakuti Yehova amene dzina lake ndi
Nsanje, ndi Mulungu wa nsanje.

15 "Musamale kuti musakachite mgwirizano ndi anthu amene akukhala
m'dziko limene mukupitalo, chifukwa iwo akamakachita zadama ndi
milungu yawo ndi kupereka nsembe, adzakuyitananii ndipo inu mudzadya
nsembe zawo. 16 Ndipo inu mukasankha ena mwa ana awo aakazi
kukhala akazi a ana anu, akaziwo akakachita zadama ndi milungu yawo,
akatsogolera ana anu aamuna kuchita chimodzimodzi.

17 "Musadzipangire milungu yosungunula.

18 "Muzichita chikondwerero cha buledi wopanda yisiti. Kwa masiku
asanu ndi awiri muzidya buledi wopanda yisiti monga momwe ndinakula-
mulirani. Muzichita zimenezi pa nthawi yoyikika mwezi wa Abibu, pakuti
mwezi umenewu inu munatuluka m'dziko la Igupto.

19 "Mwana aliyense woyamba kubadwa ndi wanga, pamodzi ndi ziweto
zoyamba kubadwa zazimuna kuchokera ku ng'ombe kapena nkhosa.
20 Muziwombola mwana woyamba kubadwa wa bulu popereka mwana
wankhosa. Mukapanda kumuwombola mupheni. Muziwombola ana anu
onse aamuna.

"Palibe ndi mmodzi yemwe adzaonekere pamaso panga wopanda
kanthu m'dzanja lake.

21 "Muzigwira ntchito masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku lachisanu
ndi chiwiri, musagwire ntchito ina iliyonse, Ngakhale nthawi yolima ndi
yokolola muyenera kupuma.

22 "Muzichita Chikondwerero cha Masabata, chifukwa ndi chikondw-
erero cha tirigu woyambirira kucha, ndiponso ndi chikondwerero cha
kututa zokolola pakutha pa chaka. 23 Amuna onse azionekera pamaso
pa Yehova Mulungu wa Israeli, katatu pa chaka. 24 Ine ndidzapirikitsa
mitundu inayo pamene inu mukufikako ndi kukulitsa malire anu. Palibe
ndi mmodzi yemwe adzafune kulanda dziko lanu ngati inu muzidzapita
katatu pa chaka pamaso pa Yehova Mulungu wanu, chaka chilichonse.

25 "Musapereke magazi anyama ngati nsembe kwa Ine pamodzi ndi
chilichonse chimene chili ndi yisiti, ndipo musasunge nsembe ya pa
Chikondwerero cha Paska mpaka mmawa.

26 “Muzibwera ndi zipatso zoyambirira kucha zabwino kwambiri ku
nyumba ya Yehova Mulungu wanu.
“Musamaphike kamwana kambuzi mu mkaka wa mayi wake.”
27 Kenaka Yehova anati kwa Mose, “Lemba mawu awa pakuti potsatira
mawuwa, ine ndipangana pangano ndi iwe ndi Israeli.” 28 Mose anakhala
kumeneko pamodzi ndi Yehova masiku 40, usana ndi usiku, wosadya
kanthu kapena kumwa madzi. Ndipo iye analemba pa miyala ija mawu a
pangano, malamulo khumi.

*Nkhope ya Mose Inyezimira*

29 Mose anatsika kuchokera m’Phiri la Sinai pamodzi ndi miyala iwiri
ija ya pangano m’manja mwake. Iye sanazindikire kuti nkhope yake
imanyezimira pakuti anayankhula ndi Yehova. 30 Aaroni ndi Aisraeli
ataona kuti nkhope ya Mose imanyezimira anaopa kumuyandikira.
31 Koma Mose anawayitana. Kotero Aaroni ndi atsogoleri onse a
gululo anabwera kwa iye, ndipo anawayankhula. 32 Kenaka Aisraeli
onse anamuyandikira, ndipo anawapatsa malamulo onse omwe Yehova
anamupatsa pa Phiri la Sinai.
33 Mose atamaliza kuyankhula nawo anaphimba nkhope yake. 34 Koma
nthawi zonse popita pamaso pa Yehova kukayankhula naye amachotsa
chophimbacho mpaka atatuluka. Ndipo akatuluka kudzawuza Aisraeli
zimene walamulidwa, 35 iwo amaona nkhope yake ikunyezimira. Choncho
Mose amaphimba nkhope yake ngakhale pamene amapita kukayankhula
ndi Yehova.

## 35

*Malamulo Osunga Sabata*

1 Mose anasonkhanitsa gulu lonse la Aisraeli ndipo anawawuza
kuti, “Zinthu zimene Yehova wakulamulirani kuti muzichite ndi izi:
2 Muzigwira ntchito zanu pa masiku asanu ndi limodzi, koma tsiku la
chisanu ndi chiwiri likhale la Sabata, tsiku lanu lopuma, lopatulika kwa
Yehova. Aliyense amene adzagwira ntchito iliyonse pa tsikuli ayenera
kuphedwa. 3 Pa tsiku la Sabata musakoleze moto paliponse pamene
mukhala.”

*Zopereka ku Malo Opatulika*

4 Mose ananena kwa gulu lonse la Aisraeli kuti, “Zimene Yehova waku-
lamulirani ndi izi: 5 Kuchokera pa zomwe muli nazo, mutenge chopereka
cha Yehova. Aliyense amene ali ndi mtima wofuna kupereka abweretse
kwa Yehova zopereka izi: Golide, siliva ndi mkuwa; 6 nsalu zobiriwira,
zapepo, zofiira, nsalu zofewa; ubweya wambuzi; 7 zikopa za nkhosa
zazimuna za utoto wofiira ndi zikopa za akatumbu; matabwa amtengo
wa mkesha, 8 mafuta anyale a olivi, zonunkhiritsa mafuta odzozera ndi
zopangira lubani wonunkhira; 9 miyala yokongola ya mtundu wa onikisi
ndi ina yabwino yoyika pa Efodi ndi pa chovala cha pachifuwa.
10 “Anthu onse aluso pakati panu abwere ndi kupanga zonse zimene
Yehova walamula: 11 Chihema ndi tenti yake ndiponso chophimba chake,
ngowe zake, maferemu ake, mitanda yake, mizati yake ndi matsinde
ake; 12 Bokosi la Chipangano pamodzi ndi mitengo yake yonyamulira
ndiponso chovundikira chake cha bokosilo ndi nsalu zophimba bokosilo;
13 tebulo pamodzi ndi mitengo yake yonyamulira pamodzi ndi zipangizo
zake zonse ndiponso buledi wokhala pamaso pa Yehova; 14 choyikapo

nyale yowunikira pamodzi ndi zipangizo zake, nyale ndi mafuta anyalezo;
15 guwa lofukizira lubani pamodzi ndi mitengo yake yonyamulira, mafuta
odzozera ndi lubani onunkhira; nsalu yotchinga pa khomo lolowera
m′chihema; 16 guwa lansembe yopsereza pamodzi ndi sefa yamkuwa,
mitengo yake yonyamulira ndi zipangizo zake zonse, beseni losambira
lamkuwa ndi miyendo yake; 17 nsalu yotchingira bwalo pamodzi ndi
mizati yake ndi matsinde ake, ndiponso nsalu yotchingira pa khomo
lolowera ku bwalo; 18 zikhomo za tenti ya chihema ndiponso za bwalo,
ndi zingwe zake; 19 zovala zolukidwa zovala potumikira kumalo opatulika,
zovala zopatulika za wansembe, Aaroni pamodzi ndi za ana ake aamuna
pamene akutumikira monga ansembe.″

20 Kenaka gulu lonse la Aisraeli linachoka pamaso pa Mose, 21 ndipo
aliyense amene anakhudzidwa mu mtima mwake nafuna kupereka,
anabwera kudzapereka chopereka kwa Yehova cha ntchito yokonza tenti
ya msonkhano, cha ntchito zonse za m′tentimo ndi cha zovala zopatulika.
22 Onse amene anali ndi mtima wofuna, amuna ndi amayi omwe anabwera
kudzapereka zodzikometsera zagolide za mtundu uliwonse: zomangira zo-
vala, ndolo, mphete ndi zokometsera. Onse anapereka golide wawo monga
nsembe yoweyula pamaso pa Yehova. 23 Aliyense amene anali ndi nsalu
ya mtundu wa mtambo, yapepo kapena yofiira kapena yofewa, yosalala,
kapena ubweya wambuzi, zikopa za nkhosa zonyika mu utoto wofiira
kapena zikopa anazibweretsa. 24 Onse amene anapereka chopereka cha
siliva kapena mkuwa anabweretsa monga chopereka kwa Yehova. Ndipo
aliyense amene anali ndi matabwa a mtengo wa mkesha kuti awagwiritse
ntchito mbali ina iliyonse ya ntchitoyo, anabweretsa. 25 Mayi aliyense
waluso analuka ndi manja ake ndi kubweretsa chomwe analuka cha
mtundu wa mtambo, chapepo kapena chofiira kapena chofewa, chosalala.
26 Ndipo amayi onse amene anali ndi mtima wofuna ndipo anali ndi
luso analuka ubweya wa mbuzi. 27 Atsogoleri anabweretsa miyala ya
onikisi ndi miyala yokongola yoyika pa efodi ndi chovala chapachifuwa.
28 Anabweretsanso zonunkhiritsa ndiponso mafuta owunikira a olivi ndi
odzozera ndi zofukizira zonunkhira. 29 Aisraeli onse aamuna ndi aakazi
amene anali ndi mtima wofuna, anabweretsa kwa Yehova chopereka
chaufulu ku ntchito yonse ya Yehova imene analamulira kudzera mwa
Mose kuti achite.

### *Bezaleli ndi Oholiabu*

30 Kenaka Mose anati kwa Aisraeli, "Taonani, Yehova wasankha Bezaleli
mwana wa Uri, mwana wa Huri, wa fuko la Yuda, 31 ndipo wamudzaza ndi
Mzimu wa Mulungu kotero kuti ali ndi luso ndi nzeru zomvetsa zinthu,
ndipo akudziwa bwino ntchito zonse zamanja monga izi: 32 Kulemba
ndondomeko ya ntchito zaluso ndi kupanga zinthu zagolide, zasiliva
ndi zamkuwa, 33 kusema ndi kuyika miyala yokongola, kukonza zinthu
zamatabwa ndiponso kugwira ntchito ina iliyonse yamanja. 34 Ndipo
Iye wapereka kwa Bezaleli pamodzi ndi Oholiabu mwana wa Ahisamaki,
wa fuko la Dani luso lophunzitsa ena. 35 Mulungu wawapatsa maluso
osiyanasiyana, maluso ogoba, olemba ndondomeko, opeta zokometsera
pa nsalu zamtundu wamtambo, zapepo ndi zofiira ndiponso zofewa
zosalala ndi zoluka. Onsewa ndi amisiri a ntchito zamanja ndi zokonza
ndondomeko.

# 36

1 Choncho Bezaleli, Oholiabu pamodzi ndi anthu aluso onse amene
Yehova anawapatsa luso ndi nzeru zodziwira kupanga zofunika zonse
zomangira malo opatulika, adzapanga zonse iwowo, monga momwe
Yehova analamulira."
2 Ndipo Mose anayitana Bezaleli ndi Oholiabu ndiponso munthu aliyense
waluso amene Yehova anamupatsa luso ndiponso amene anali ndi
mtima wofuna kugwira ntchito. 3 Iwo analandira kuchokera kwa Mose
zopereka zonse Aisraeli anabweretsa kuti agwirire ntchito yomanga malo
wopatulika. Ndipo anthu anapitirira kupereka zopereka zaufulu mmawa
uliwonse. 4 Kotero amisiri onse amene amagwira ntchito yonse ya
malo wopatulika anasiya ntchitoyo 5 ndipo anati kwa Mose, "Anthu
akubweretsa kuposa zimene zikufunika kugwirira ntchito imene Yehova
analamulira kuti ichitike."
6 Choncho Mose analamulira ndipo analengeza mu msasa onse, "Mwa-
muna kapena mayi aliyense asaperekenso chopereka chilichonse cha ku
malo wopatulika." Choncho anthu analetsedwa kubweretsa zambiri,
7 chifukwa zimene anali nazo zinali zoposera zimene zimafunika kug-
wirira ntchito yonse.

*Chihema*

8 Anthu onse aluso pakati pa anthu ogwira ntchitoyo anapanga chihema
pogwiritsa ntchito nsalu khumi zofewa, zosalala ndi zolukidwa bwino,
zobiriwira, zapepo ndi zofiira. Ndipo anthu aluso anapeta pa nsaluzo
Akerubi. 9 Nsalu zonse zinali zofanana. Mulitali mwake zinali mamita
khumi ndi atatu, mulifupi mamita awiri. 10 Iwo analumikiza nsalu
zisanu, kuti ikhale nsalu imodzi ndipo anachita chimodzimodzi ndi nsalu
zisanu zinazo. 11 Kenaka anapanga zokolowekamo za nsalu yobiriwira
m'mphepete mwa nsalu imodzi yotsiriza ya mbali ina. Ndipo anachita
chimodzimodzi ndi nsalu yotsiriza ya mbali inayo. 12 Iwo anasokerera
zokolowekamo makumi asanu pa nsalu yoyamba ndi zokolowekamo
makumi asanu zinanso pa nsalu inayo. Anapanga kuti zokolowekamozo
ziziyang'anana. 13 Kenaka anapanga ngowe zagolide 50 zolumikizira nsalu
ziwirizo kotero kuti zinapanga chihema chimodzi.
14 Iwo anapanga nsalu za ubweya wambuzi zophimba pamwamba
pa chihemacho. Nsalu zonse pamodzi zinalipo khumi ndi imodzi.
15 Nsalu zonse khumi ndi imodzi zinali zofanana. Mulitali mwake
munali mamita khumi ndi anayi ndipo mulifupi mwake munali mamita
awiri. 16 Iwo analumikiza nsalu zisanu kukhala nsalu imodzi ndipo
nsalu zinazo zisanu ndi imodzi, analumikizanso kukhala nsalu imodzinso.
17 Kenaka anasokerera zokolowekamo makumi asanu m'mphepete mwa
nsalu imodzi yotsirizira ya nsalu yoyamba yolumikiza ija ndiponso
anapanga zokolowekamo zina makumi asanu m'mphepete mwa nsalu
yotsirizira ya nsalu inanso yolumikiza ija. 18 Iwo anapanga ngowe 50
zamkuwa zolowetsa mu zokolowekazo ndipo anaphatikiza nsalu ziwirizo
kuti tentiyo ikhale imodzi. 19 Ndipo anapanga chikopa cha nkhosa
zazimuna cha utoto wofiira chophimbira tentiyo ndipo pamwamba pake
anapanganso chophimbira china cha zikopa za akatumbu.
20 Iwo anapanga maferemu amatabwa amtengo wa mkesha oyimikira
chihemacho. 21 Feremu iliyonse inali yotalika mamita anayi ndipo muli-
fupi mwake munali masentimita 69. 22 Thabwa lililonse linali ndi zolumik-
izira ziwiri. Iwo anapanga maferemu onse a chihemacho ndi matabwa

otere. 23 Anapanga maferemu makumi awiri a mbali yakummwera kwa
chihemacho, 24 ndiponso anapanga matsinde 40 asiliva ndipo anawayika
pansi pa maferemuwo. Pansi pa feremu iliyonse anayika matsinde
awiri ogwiriziza zolumikizira ziwiri zija. 25 Iwo anapanganso maferemu
makumi awiri a mbali yakumpoto ya chihemacho, 26 ndiponso matsinde
makumi anayi asiliva, awiri pansi pa feremu iliyonse. 27 Anapanganso
maferemu asanu ndi imodzi a kumbuyo kwa tenti, kumbali yakumadzulo,
28 ndiponso maferemu awiri a pa ngodya yakumbuyo kwenikweni kwa
tenti. 29 Pa ngodya ziwirizi panali maferemu awiri, kuyambira pansi
mpaka pamwamba atalumikizidwa pa ngowe imodzi. Maferemu onse
anali ofanana. 30 Choncho panali maferemu asanu ndi atatu ndiponso
matsinde 16 asiliva, awiri anali pansi pa feremu iliyonse.

31 Iwo anapanganso mitanda ya matabwa amtengo wa mkesha. Mitanda
isanu inali ya maferemu a mbali imodzi ya chihema, 32 mitanda isanu
inanso inali ya maferemu a mbali inayo ndipo mitanda ina isanu ya
mbali yakumadzulo, kumapeto kwenikweni kwa chihema. 33 Anapanga
mtanda wapakati omwe umachokera pa maferemu a mbali ina mpaka
mbali inanso. 34 Iwo anakuta maferemuwo ndi golide ndiponso anapanga
mphete zagolide zogwiriziza mitandayo. Ndipo mitandayonso anayikuta
ndi golide.

35 Anapanga nsalu yokhala ndi mtundu wamtambo, wapepo ndi ofiira
ndipo nsaluyo inali yolukidwa bwino, yofewa ndi yosalala. Ndipo anthu
aluso anapetapo zithunzi za Akerubi. 36 Iwo anapanga nsanamira zinayi
zamtengo wa mkesha zokutidwa ndi golide. Anapanganso ngowe zagolide
za nsanamirazo ndi matsinde asiliva anayi. 37 Anapanga nsalu ya pa
chipata cholowera mu chihema, yamtundu wamtambo, wapepo ndi ofiira
yomwe inali yofewa ndi yosalala, yopetedwa bwino ndi amisiri aluso.
38 Anapanga nsanamira zisanu ndi ngowe zake. Anakuta pamwamba pa
nsanamirazo ndi zomangira zake ndi golide, ndipo anapanganso matsinde
asanu amkuwa.

# 37

*Bokosi la Chipangano*

1 Bezaleli anapanga Bokosi la Chipangano lamatabwa amtengo wa
mkesha. Kutalika kwake kunali masentimita 114, mulifupi mwake
munali masentimita 69, msinkhu wake masentimita 69. 2 Iye analikuta
bokosilo ndi golide wabwino kwambiri m'kati mwake ndi kunja komwe.
Anapanganso mkombero wagolide kuzungulira bokosilo. 3 Iye anapanga
mphete zinayi zagolide ndi kuzimangirira ku miyendo yake inayi ija, mbali
ina ziwiri ndi mbali inanso ziwiri. 4 Kenaka anapanga mizati yamtengo wa
mkesha ndi kuzikuta ndi golide. 5 Ndipo analowetsa nsichizo m'mphete
zija za mbali zonse ziwiri za bokosilo kuti azinyamulira.

6 Iye anapanga chivundikiro cha bokosilo cha golide wabwino kwambiri,
kutalika kwake masentimita 114, mulifupi mwake masentimita 69. 7 Ndipo
anapanga Akerubi awiri agolide osula ndi nyundo ndi kuwayika mbali
ziwiri za chivundikirocho. 8 Iye anapanga kerubi mmodzi mbali ina ndi
wina mbali inayo. Akerubiwa anawapangira limodzi ndi chivundikirocho
m'mapeto mwa mbali ziwirizo. 9 Mapiko a Akerubiwo anatambasukira
pamwamba pa chivundikiro cha bokosilo kuti achiphimbe. Akerubiwo
anakhala choyang'anana, aliyense kuyang'ana chivundikirocho.

*Mapangidwe a Tebulo*

10 Iwo anapanga tebulo la matabwa amtengo wa mkesha, mulitali
mwake masentimita 91, mulifupi mwake masentimita 46, msinkhu wake
masentimita 69. 11 Kenaka analikuta ndi golide wabwino kwambiri, ndipo
anapanga mkombero wagolide m'mbali mwake. 12 Iwo anapanga feremu
yozungulira tebulo, mulifupi mwake ngati chikhatho cha dzanja, ndipo
anayika mkombero wagolide kuzungulira feremuyo. 13 Iwo anapanga
mphete zinayi zagolide ndipo anazilumikiza ku ngodya zake zinayi,
kumene kunali miyendo yake inayi. 14 Mphetezo anaziyika kufupi ndi
feremu kuti azikolowekamo nsichi zonyamulira tebuloyo. 15 Anapanga
nsichi zamtengo wa mkesha ndi kuzikuta ndi golide kuti azinyamulira
tebulolo. 16 Ndipo anapanga ziwiya za pa tebulolo zagolide wabwino,
mbale ndi zipande, mitsuko ndi mabeseni zogwiritsa ntchito popereka
nsembe za chakumwa.

*Mapangidwe a Choyikapo Nyale*

17 Iwo anapanga choyikapo nyale chagolide wabwino kwambiri. Tsinde
lake ndi mphanda zake zinasulidwa ndi nyundo. Zikho zake zokhala ndi
mphukira ndi maluwa ake zinapangidwa kumodzi. 18 M'mbali mwake
munali mphanda zisanu ndi imodzi, zitatu mbali iliyonse. 19 Zikho
zitatu zokhala ngati za maluwa amtowo, mphukira ndi duwa zinali pa
mphanda yoyamba. Pa mphanda yachiwiri panalinso zikho zitatu zokhala
ngati za maluwa amtowo, mphukira ndi duwa. Ndipo mphanda zonse
zisanu ndi imodzi zinali chimodzimodzi ndipo zinatuluka m'choyikapo
nyalecho. 20 Pa choyikapo nyalecho panali zikho zinayi zokhala ngati
maluwa amtowo, mphukira ndi maluwa ake. 21 Mphukira yoyamba inali
m'munsi mwa nthambi ziwiri zoyamba za pa choyikapo nyale. Mphukira
yachiwiri inali m'munsi mwa nthambi ziwiri zinazo. Mphukira yachitatu
inali m'munsi mwa nthambi zina ziwirinso. Zonse pamodzi zinali nthambi
zisanu ndi imodzi 22 Mphukira ndi nthambi zonse zinasulidwa kumodzi
ndi choyikapo nyalecho ndi golide wabwino kwambiri.
23 Iwo anapanga nyale zisanu ndi ziwiri, mbaniro ndi zowolera phulusa,
zonse zinali zagolide wabwino kwambiri. 24 Iwo anapanga choyikapo
nyale ndi zipangizo zake zonse zagolide wabwino kwambiri wolemera
makilogalamu 34.

*Guwa Lofukizirapo Lubani*

25 Iwo anapanga guwa lamatabwa amtengo wa mkesha lofukizirapo
lubani. Linali lofanana mbali zonse, mulitali masentimita 46, mulifupi
masentimita 46, ndipo msinkhu masentimita 91, ndipo nyanga zake
zinapangidwa kumodzi ndi guwalo. 26 Iwo anakuta guwa lonse ndi golide
wabwino kwambiri, pamwamba pake, mbali zonse ndi nyanga zake, ndipo
anapanga mkombero wagolide kuzungulira guwalo. 27 Anapanga mphete
ziwiri pansi pa mkomberowo ndi kulumikiza ku mbali zonse ziwiri kuti
apisemo nsichi zonyamulira. 28 Anapanga mizati yamtengo wa mkesha
ndipo anayikuta ndi golide.
29 Iwo anapanganso mafuta opatulika odzozera ndi zofukiza za fungo
lokoma kwambiri. Iyi inali ntchito ya m'misiri waluso lopanga zonunkhir-
itsa.

# 38

*Guwa Lansembe Yopsereza*

1 Anapanga guwa lansembe zopsereza lamatabwa amtengo wa mke-
sha. Linali lofanana mbali zonse. Msinkhu wake masentimita 137,
mulitali mwake masentimita 229, mulifupi masentimita 229. 2 Anapanga
nyanga imodziimodzi pa ngodya zake zinayizo, kotero kuti nyangazo
ndi guwalo zinali chinthu chimodzi, ndipo anakuta guwalo ndi mkuwa.
3 Anapanganso ziwiya zamkuwa izi zogwirira ntchito pa guwalo: miphika,
mafosholo, mabeseni owazira magazi, ngowe zokowera nyama ndi
zosonkhezera moto. 4 Anapanga sefa yachitsulo chamkuwa ya guwa
lansembelo kuti ikhale mmunsi mwa khoma la guwa lansembelo, ku-
chokera pansi mpaka pakati pa khoma la guwalo. 5 Anapanga mphete
zamkuwa zinayi ndipo anazilumikiza ku ngodya zinayi za sefa ija kuti
zigwire nsichi zonyamulira. 6 Anapanga nsichi zamtengo wa mkesha
ndipo anazikuta ndi mkuwa. 7 Iwo analowetsa nsichizo m'mphetemo
mbali zonse ziwiri za guwalo kuti azinyamulira. Guwalo linali lamatabwa
ndi logoba m'kati mwake.

### *Beseni Losambira*

8 Anapanga beseni lamkuwa lokhala ndi miyendo yamkuwanso kuchok-
era ku magalasi oyang'anira nkhope a amayi amene ankatumikira pa
chipata cha tenti ya msonkhano.

### *Bwalo la Chihema*

9 Kenaka anapanga bwalo la chihema. Mbali yakummwera inali yotalika
mamita 46 ndipo kunali nsalu yotchinga yofewa yosalala yolukidwa
bwino. 10 Anapanganso mizati makumi awiri, matsinde makumi awiri
amkuwa ndi ngowe zasiliva ndi zingwe za mizatiyo. 11 Mbali yakumpoto
inalinso yotalika mamita 46 ndipo inali ndi mizati makumi awiri, matsinde
amkuwa makumi awiri, ngowe zasiliva ndi zingwe za mizatiyo.

12 Mbali yakumadzulo inali yotalika mamita 23 ndipo inali ndi nsalu
yotchinga, mizati khumi ndi matsinde khumi. Inalinso ndi ngowe
zasiliva ndi zingwe za mizatiyo. 13 Mbali yakummawa, kotulukira dzuwa,
inalinso yotalika mamita 23. 14 Mbali imodzi yachipata kunali nsalu
yotchinga yotalika mamita asanu ndi awiri, mizati itatu ndi matsinde
atatu, 15 polowera m'bwalo panali nsalu yotchinga ya mamita asanu
ndi awiri pamodzi ndi mizati itatu ndi matsinde atatu. 16 Katani yonse
yotchinga kuzungulira chihema inali yofewa, yosalala ndi yolukidwa
bwino. 17 Matsinde amizati anali amkuwa. Ngowe ndi zingwe za mizati
zinali zasiliva, ndipo pamwamba pa mizatiyo anakutapo siliva. Choncho
mizati yonse ya bwalolo inalumikizidwa ndi zingwe zasiliva.

18 Nsalu yotchinga ya pa chipata inali yamtundu wa mtambo, yapepo ndi
yofiira, yofewa yosalala ndi yopangidwa ndi anthu aluso. Nsaluyo inali
yotalika mamita asanu ndi anayi, molingana ndi nsalu zotchinga bwalo.
Msinkhu wake unali masentimita 229, 19 pamodzi ndi mizati yake inayi ndi
matsinde amkuwa anayi. Ngowe ndi zingwe zake zinali za siliva, ndipo
pamwamba pake pa mzati anakutapo ndi siliva. 20 Zikhomo za chihema
ndi zina zonse zozungulira chihemacho zinali zamkuwa.

### *Zipangizo Zachitsulo za ku Malo Opatulika*

21 Chiwerengero cha zipangizo zimene anagwiritsa ntchito popanga
chihema, chihema chaumboni, zimene Mose analamulira Alevi kuti
alembe motsogozedwa ndi Itamara mwana wa Aaroni, wansembe, chinali
ichi: 22 Bezaleli mwana wa Uri, mwana wa Huzi wa fuko la Yuda anapanga

chilichonse Yehova analamulira Mose, 23 pamodzi ndi Oholiabu mwana
wa Ahisamaki, wa fuko la Dani, wa luso la zopangapanga ndi kulemba
mapulani, ndi wopanga nsalu zolukidwa bwino za mtundu wa mtambo,
yapepo ndi zofiira, zofewa ndi zosalala. 24 Golide yense wochokera ku
nsembe yoweyula amene anagwiritsa ntchito pa ntchito yonse yopanga
malo wopatulika anali wolemera makilogalamu 1,000 potsata miyeso ya
kumalo wopatulika.

25 Siliva wochokera ku gulu lonse la anthu anali wolemerera makilo-
galamu 3,430, potsata miyeso ya ku malo wopatulika. 26 Munthu aliyense
amapereka beka imodzi, kufanana ngati makilogalamu 6, potsata muyeso
wa ku malo wopatulika. Kuchokera kwa aliyense amene anawerengedwa
kuyambira zaka 20 kapena kuposerapo, amuna onse analipo 603,550.
27 Anagwiritsa ntchito siliva wolemera makilogalamu 3,400 kupanga
matsinde 100 a ku malo wopatulika ndi makatani, ndipo makilogalamu
34 kupanga tsinde limodzi. 28 Makilogalamu otsalawo anagwiritsa ntchito
popanga ngowe zamzati kukutira pamwamba pa mizati ndiponso kupanga
zingwe zake.

29 Mkuwa ochokera ku nsembe yoweyula unali makilogalamu 2,425.
30 Iwo anawugwiritsa ntchito popanga matsinde a pa chipata cha tenti
ya msonkhano, guwa la mkuwa pamodzi ndi sefa yake ndiponso ziwiya
zonse, 31 matsinde ozungulira bwalo ndiponso a pa chipata pake, ndi
zikhomo zonse za tentiyo ndi matsinde a malo wozungulirapo.

# 39

*Zovala za Ansembe*

1 Anapanga zovala za ansembe, zovala potumikira ku malo wopatulika
pogwiritsa ntchito nsalu ya mtundu wa mtambo, yapepo ndi yofiira. Ana-
panganso zovala zopatulika za Aaroni monga momwe Yehova analamulira
Mose.

*Chovala cha Efodi*

2 Popanga efodi, iwo anagwiritsa ntchito golide, nsalu yamtundu wa
mtambo, yapepo, yofiira, yosalala yofewa. 3 Anasula golide wopyapyala
ndi kumulezaleza kuti alumikize kumodzi ndi nsalu yamtundu wa
mtambo, yapepo ndi yofiira yosalala yofewa yolukidwa mwaluso. 4 Iwo
anapanga efodi imene inali ndi timalamba tiwiri ta pa mapewa, tosokerera
ku msonga zake ziwiri kuti azitha kumanga. 5 Lamba womangira efodi
anali wolukidwa mwaluso ngati efodiyo. Anali nsalu imodzi ndi efodiyo,
wopangidwa ndi golide, nsalu yamtundu wa mtambo, yapepo, yofiira,
yofewa yosalala, monga momwe Yehova analamulira Mose.

6 Iwo anakonza miyala ya onikisi ndi kuyiika mu zoyikamo zake zagolide
ndipo anazokota mayina a ana a Israeli monga amachitira pa chidindo.
7 Kenaka anayimangirira pa tinsalu ta m'mapewa ta efodi tija ngati miyala
ya chikumbutso cha ana a Israeli monga momwe Yehova analamulira
Mose.

*Chovala Chapachifuwa*

8 Iwo anapanga chovala chapachifuwa mwaluso kwambiri.
Anachipanga ngati efodi pogwiritsa ntchito golide, nsalu yamtundu
wa mtambo, yapepo, yofiira, yofewa yosalala ndi yolukidwa bwino.
9 Kutalika kwake kunali kofanana mbali zonse, mulitali masentimita 23,

mulifupi masentimita 23, chinali chopinda pawiri. 10 Kenaka anayikapo
mizere inayi ya miyala yokongola kwambiri. Mzere woyamba anayika
miyala ya rubi, topazi ndi berili; 11 mzere wachiwiri anayikapo miyala ya
emeradi, safiro ndi dayimondi; 12 mzere wachitatu anayikapo miyala ya
opera, agate ndi ametisiti; 13 mzere wachinayi anayikapo miyala ya topazi,
onikisi ndi yasipa. Miyalayi anayiyika mu zoyikamo zagolide. 14 Miyalayo
inalipo khumi ndi iwiri, uliwonse kuyimira dzina limodzi la ana a Israeli.
Mwala uliwonse unazokotedwa ngati chidindo dzina limodzi la mafuko
khumi ndi awiri a Israeli.

15 Anapanga timaunyolo tagolide wabwino kwambiri ta pa chovala
chapachifuwa, topota ngati chingwe. 16 Anapanganso zoyikamo zake
zagolide ndi mphete ziwiri zagolide, ndipo anamangirira mphetezo pa
ngodya ziwiri za chovala chapachifuwa. 17 Anamangirira timaunyolo
tiwiri tagolide tija pa mphete za pa ngodya pa chovala chapachifuwacho.
18 Ndipo mbali ina ya timaunyoloto anamangirira pa zoyikapo zake
ziwiri zija, ndi kulumikiza pa tinsalu takutsogolo kwa mapewa a efodi.
19 Anapanganso mphete ziwiri zagolide ndipo analumikiza ku ngodya
ziwiri zam'munsi mwa chovala chapachifuwa, champhepete mwake,
m'kati pafupi ndi efodi ija. 20 Kenaka anapanga mphete zina ziwiri
zagolide ndi kuzilumikiza kumunsi kwa tinsalu takutsogolo kwa efodi,
pafupi ndi msoko, pamwamba pang'ono pa lamba wam'chiwuno wa efodi.
21 Anamangirira mphete za pa chovala chapachifuwa zija ku mphete za
efodi ndi chingwe chamtundu wa mtambo, kulumikiza lamba ndi chovala
chapachifuwacho kuti chovala chapachifuwacho chisalekane ndi efodi ija
monga Yehova analamulira Mose.

### *Zovala zina za Unsembe*

22 Anayipangira efodiyo mkanjo wamtundu wa mtambo, wolukidwa
ndi mmisiri waluso. 23 Mkanjowo unali ndi malo opisapo mutu pakati
pakepo. Pa chibowopo panali chibandi chosokedwa mochita ngati kuluka
monga muja akhalira malaya kuti chibowocho chilimbe, chisang'ambike.
24 Pa mpendero wam'munsi wa mkanjowo, analumikiza mphonje zokhala
ngati makangadza za nsalu yamtundu wa mtambo, yapepo ndi yofiira
yofewa yosalala ndi yopetedwa bwino yomwe inazungulira mkanjo.
25 Ndipo anapanga maberu agolide wabwino kwambiri ndipo analumikiza
mozungulira mpendero pakati pa makangadzawo. 26 Kotero panali
mphonje imodzi ndi belu limodzi kuzungulira mpendero wa mkanjo
wovala potumikira monga momwe Yehova analamulira Mose.

27 Kwa Aaroni ndi ana ake anawapangira minjiro ya nsalu yofewa
yosalala, yolukidwa bwino ndi munthu waluso, 28 nduwira ya nsalu
yofewa yosalala, lamba wa nsalu yofewa yosalala, womanga m'mutu,
ndi makabudula am'kati a nsalu yofewa yosalala olukidwa bwino.
29 Anapanga lamba wolukidwa bwino wa nsalu yofewa ndi yosalala ya
mtundu wa mtambo yapepo ndi yofiira. Ili linaliluso la munthu wopanga
zokometsera monga Yehova analamulira Mose.

30 Iwo anapanga duwa lagolide wabwino kwambiri ngati chidindo ndipo
anazokotapo mawu akuti, WOPATULIKIRA YEHOVA. 31 Kenaka analimangira
ndi chingwe cha nsalu yamtundu wa mtambo pa nduwira, monga momwe
Yehova analamulira Mose.

### *Mose Ayendera Chihema*

32 Tsopano ntchito yonse ya tenti ya msonkhano inatha. Aisraeli
anachita zonse monga momwe Yehova analamulira Mose. 33 Kenaka
anabweretsa chihema kwa Mose. Tenti ndi zipangizo zake, ngowe
zake, maferemu ake, mitanda yake, mizati yake ndi matsinde ake;
34 chophimba cha chikopa cha nkhosa yayimuna chonyikidwa mu utoto
ofiira, chophimba cha chikopa cha akatumbu ndi nsalu zophimba;
35 bokosi la umboni pamodzi ndi mitengo yake yonyamulira ndiponso
chovundikira chake; 36 tebulo pamodzi ndi zipangizo zake ndiponso
buledi wokhala pamaso pa Yehova; 37 choyikapo nyale chagolide wabwino
kwambiri pamodzi ndi nyale zake ndi zipangizo zake zonse, ndiponso
mafuta anyalezo; 38 guwa lagolide, mafuta odzozera, lubani onunkhira ndi
nsalu yotchinga pa khomo lolowera mu tenti; 39 guwa lamkuwa ndi sefa
yamkuwa, mitengo yake yonyamulira ndi zipangizo zake zonse; beseni ndi
miyendo yake; 40 nsalu yotchingira bwalo pamodzi ndi mizati yake ndi
matsinde ake ndiponso nsalu yotchingira pa khomo lolowera ku bwalo;
zingwe zake ndi zikhomo za tenti; zipangizo zonse za chihema, tenti
ya msonkhano; 41 ndiponso zovala zolukidwa zovala potumikira kumalo
opatulika, zovala zopatulika za wansembe, Aaroni pamodzi ndi za ana ake
aamuna pamene akutumikira monga ansembe.

42 Aisraeli anagwira ntchito yonse monga momwe Yehova analamulira
Mose. 43 Mose anayendera ntchitoyo ndipo anaona kuti anayichita monga
momwe Yehova analamulira. Kotero Mose anawadalitsa.

# 40

*Adzutsa Chihema*

1 Kenaka Yehova anati kwa Mose, 2 "Imika chihema, tenti ya msonkhano,
tsiku loyamba la mwezi. 3 Uyikemo bokosi la umboni ndipo uphimbe
bokosilo ndi katani. 4 Ulowetsemo tebulo ndi kuyika zimene zimakhala
pamenepo. Kenaka ulowetse choyikapo nyale ndipo uyikepo nyale zake.
5 Uyike guwa lofukiza la golide patsogolo pa bokosi la umboni ndipo uyike
katani ya pa chipata cha chihema.

6 "Uyike guwa lansembe yopsereza patsogolo pa chipata cha chihema,
tenti ya msonkhano. 7 Uyike beseni pakati pa tenti ya msonkhano ndi guwa
lansembe ndipo uyikemo madzi. 8 Upange bwalo lozungulira chihemacho
ndipo uyike katani ya pa chipata cha bwalolo.

9 "Utenge mafuta wodzozera ndipo udzoze chihema ndi chilichonse
chili m'menemo ndipo zidzakhala zoyeretsedwa. 10 Kenaka udzoze guwa
lansembe lopsereza ndi ziwiya zake zonse. Ulipatule guwalo ndipo
lidzakhala loyera kwambiri. 11 Udzoze beseni ndi miyendo yake ndipo
uzipatule.

12 "Ubwere ndi Aaroni ndi ana ake pa chipata cha tenti ya msonkhano
ndipo uwasambitse ndi madzi. 13 Kenaka umuveke Aaroni zovala zopat-
ulika, umudzoze ndi kumupatula kotero kuti athe kunditumikira monga
wansembe. 14 Ubweretse ana ake ndipo uwaveke minjiro. 15 Uwadzoze
monga momwe unadzozera abambo awo, kotero kuti anditumikire monga
ansembe. Kudzozedwako kudzakhala unsembe wawo pa mibado ndi
mibado" 16 Mose anachita zonse monga Yehova anamulamulira.

17 Kotero anayimika chihema tsiku loyamba la mwezi woyamba m'chaka
chachiwiri. 18 Nthawi imene Mose anayimika chihema, anayika matsinde
m'malo ake, kuyimitsa maferemu, kulowetsa mitanda ndi kuyika nsichi.

19 Kenaka anayika tenti pamwamba pa chihema ndipo anayika chophimba
pa tenti monga momwe Yehova analamulira Mose.
20 Iye anatenga miyala ya umboni nayika m'bokosi lija ndi kuyika
chivundikiro pamwamba pake. 21 Kenaka analowetsa bokosilo m'chihema
ndipo anapachika katani ndi kubisa bokosi la umboni monga momwe
Yehova analamulira iye.
22 Mose anayika tebulo mu tenti ya msonkhano kumpoto kwa chihema,
kunja kwa katani, 23 ndipo anayikapo buledi pamaso pa Yehova, monga
momwe Yehova analamulira Mose.
24 Iye anayikanso choyikapo nyale mu tenti ya msonkhano
moyang'anana ndi tebulo mbali yakummwera kwa chihema. 25 Ndipo
anayikapo nyale zija pamaso pa Yehova, monga Yehova analamulira Mose.
26 Mose anayika guwa la golide mu tenti ya msonkhano patsogolo
pa katani 27 ndipo anapserezapo lubani wonunkhira monga Yehova
anamulamulira. 28 Kenaka anayika katani ya pa chipata cha chihema.
29 Iye anayika guwa lansembe yopsereza pafupi ndi chipata cha
chihema, tenti ya msonkhano, ndipo anapereka nsembe yopsereza ndi
nsembe ya ufa monga Yehova anamulamulira.
30 Iye anayika beseni pakati pa tenti ya msonkhano ndi guwa lansembe
ndipo anathiramo madzi wosamba, 31 ndipo Mose, Aaroni ndi ana ake
amasamba manja ndi mapazi awo. 32 Iwo amasamba nthawi zonse
akamalowa mu tenti ya msonkhano kapena kuyandikira guwa lansembe
monga Yehova analamulira Mose.
33 Kenaka Mose anamanga bwalo kuzungulira chihema ndi guwa
lansembe ndipo anayika katani ya pa chipata cha bwalo. Kotero Mose
anamaliza ntchito.

### *Ulemerero wa Yehova*

34 Kenaka mtambo unaphimba tenti ya msonkhano, ndipo ulemerero
wa Yehova unadzaza m'chihemacho. 35 Mose sanathe kulowa mu tenti ya
msonkhano chifukwa mtambo unali utakhazikika pa chihemacho, ndipo
ulemerero wa Yehova unadzaza m'chihemacho.
36 Pa maulendo awo onse, mtambo ukachoka pamwamba pa chihema,
Aisraeli ankasamukanso pamene analipo. 37 Koma ngati mtambo suna-
choke, iwo sankasamukanso mpaka tsiku limene udzachoke. 38 Kotero
mtambo wa Yehova unkakhala pamwamba pa chihema usana, ndi
mtambo wamoto umakhala usiku, pamaso pa nyumba yonse ya Israeli
pa masiku onse aulendo wawo.

# Levitiko

*Nsembe Zopsereza*
1 26 Yehova anayitana Mose mu tenti ya msonkhano. Iye anati,
2 “Aliyense wa inu ngati abwera ndi nsembe kwa Yehova kuchokera pa
ziweto zake, choperekacho chikhale ng’ombe, nkhosa kapena mbuzi.
3 “ ‘Ngati munthu apereka nsembe yopsereza ya ng’ombe, ikhale
yayimuna yopanda chilema. Aziyipereka pa khomo la tenti ya msonkhano,
kuti Yehova alandire. 4 Munthuyo asanjike dzanja lake pa mutu pa nsembe
yopserezayo, ndipo idzalandiridwa kuti ikhale yopepesera machimo ake.
5 Pambuyo pake aphe ng’ombeyo pamaso pa Yehova, ndipo ansembe, ana
a Aaroni, atenge magazi ake ndi kuwawaza mbali zonse za guwa lansembe
limene lili pa khomo la tenti ya msonkhano. 6 Munthuyo asende nsembe
yopserezayo ndi kuyidula nthulinthuli. 7 Ndipo ana a Aaroni, wansembe
uja asonkhe moto pa guwa ndi kuyalapo nkhuni pa motopo. 8 Kenaka
ana a Aaroni, wansembe uja, ayike nthuli za nyamayo, mutu wake
pamodzi ndi mafuta omwe pa nkhuni zimene zili paguwapo. 9 Munthuyo
atsuke zam’kati mwa nyamayo pamodzi ndi miyendo yake yomwe, ndipo
wansembe awotche nyama yonse paguwapo. Iyi ndi nsembe yopsereza,
chopereka chowotcha pa moto, cha fungo lokomera Yehova.
10 “ ‘Koma ngati chopereka cha nsembe yopserezayo ndi nkhosa kapena
mbuzi kuchokera pa ziweto zake, munthuyo apereke yayimuna yopanda
chilema. 11 Ayiphere kumpoto kwa guwa, pamaso pa Yehova, ndipo ana
a Aaroni amene ndi ansembe, awaze magazi ake mbali zonse za guwalo.
12 Kenaka ayidule nyamayo nthulinthuli, ndipo wansembe ayike nthulizo
pa guwa, atengenso mutu ndi mafuta omwe, ndipo ayike zonsezi pa
nkhuni zimene zikuyaka pa guwa. 13 Munthuyo atsuke zam’kati mwa
nyamayo pamodzi ndi miyendo yake yomwe, ndipo wansembe abwere
nazo zonse ndi kuzitentha pa guwa. Iyi ndi nsembe yopsereza, chopereka
chotentha pa moto, fungo lokomera Yehova.
14 “ ‘Koma ngati chopereka kwa Yehova ndi nsembe yopsereza ya
mbalame, ndiye ikhale njiwa kapena mawunda. 15 Wansembe abwere
nayo ku guwa, ayidule mutu moyipotola ndi kutentha mutuwo pa guwa.
Magazi ake awathire pansi kuti ayenderere pambali pa guwa. 16 Iye
achotse chithokomiro pamodzi ndi nthenga zake zomwe ndi kuzitaya ku
malo wotayirako phulusa, kummawa kwa guwalo. 17 Kenaka aying’ambe
pakati, koma asachotse mapiko. Ndipo wansembe ayiwotche pa nkhuni
zimene zikuyaka pa guwa. Imeneyi ndi nsembe yopsereza, yowotcha pa
moto ndiponso ya fungo lokomera Yehova.

## 2

*Nsembe Zachakudya*
1 “ ‘Munthu wina aliyense akabwera ndi nsembe ya chakudya kwa
Yehova, chopereka chake chizikhala ufa wosalala. Ufawo ausakanize
ndi mafuta ndi lubani, 2 ndipo apite nawo kwa ansembe, ana a Aaroni.
Atapeko modzazitsa dzanja ufa wosalala uja kuti ukhale wachikumbutso
pamodzi ndi mafuta ndi lubani ndipo atenthe zonsezi pa guwa lansembe
kuti zilandiridwe ndi Yehova m’malo mwa chopereka chonse. Iyi ndi

nsembe yotentha pa moto ndiponso fungo lokomera Yehova. 3 Zotsala za
nsembe ya chakudyazo ndi za Aaroni pamodzi ndi ana ake. Chimenechi
ndi chigawo chopatulika kwambiri chifukwa chatapidwa pa chopereka
chotentha pa moto cha Yehova.

4 “ ‘Ukabweretsa nsembe ya chakudya chophika mu uvuni, ikhale ya
buledi wa ufa wosalala wopanda yisiti koma wosakaniza ndi mafuta,
kapena timitanda ta buledi topyapyala, topanda yisiti koma topaka mafuta.
5 Ngati nsembe yako yachakudya ndi yophika pa chitsulo chamoto,
ikhale ya buledi wa ufa wosalala wopanda yisiti koma wosakaniza ndi
mafuta. 6 Umuduledule bulediyo ndi kumupaka mafuta; imeneyo ndi
nsembe yachakudya. 7 Ngati nsembe yako yachakudya ndi yophikidwa
pa chiwaya, ikhale ya buledi wa ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta.
8 Munthu azibwera ndi nsembe za chakudya zimene wapanga ndi
zinthu zimenezi. Atachipereka kwa wansembe, iyeyu adzipita nacho
ku guwa. 9 Wansembeyo atengeko gawo lina la nsembeyo kukhala ufa
wachikumbutso kuti ilandiridwe ndi Yehova m’malo mwa nsembe yonse
ndipo ayitenthe pa moto monga nsembe yopsereza ya fungo lokomera
Yehova. 10 Zotsala za nsembe ya chakudyayo zikhale za Aaroni ndi ana
ake. Chimenechi ndi chigawo chopatulika kwambiri chifukwa chatapidwa
pa chopereka chotentha pa moto cha Yehova.

11 “ ‘Nsembe ya chakudya chilichonse imene ubweretsa kwa Yehova
ikhale yopanda yisiti, pakuti suyenera kupereka kwa Yehova nsembe
yotentha pa moto imene ili ndi yisiti kapena uchi. 12 Ziwirizi ungathe kub-
wera nazo kwa Yehova ngati chopereka cha zokolola zoyambirira. Koma
usazitenthe pa guwa kuti zikhale fungo lokomera Yehova. 13 Zopereka
zako zonse zachakudya uzithire mchere. Usayiwale kuthira mchere
pa chopereka chako popeza mcherewo ukusonyeza pangano pakati pa
iwe ndi Mulungu wako. Tsono uzinthira mchere pa chopereka chako
chilichonse.

14 “ ‘Mukamapereka kwa Yehova chopereka cha chakudya choyamba
kucha, choperekacho chikhale cha chipatso chatsopano chokazinga pa
moto ndi chopunthapuntha. 15 Uchithire mafuta ndi lubani pakuti ndi
chopereka cha chakudya. 16 Tsono wansembe atenthe gawo la chopereka
chopunthapuntha chija kuti chikhala ufa wachikumbutso ndi cha mafuta
pamodzi ndi lubani yense kuti Yehova alandire m’malo mwa zopereka
zonse. Ichi ndi chopereka chotentha pa moto cha Yehova.

# 3

*Nsembe Yachiyanjano*

1 “ ‘Ngati munthu apereka nsembe ya chiyanjano kwa Yehova, ndipo
choperekacho n’kukhala ng’ombe yayimuna kapena yayikazi, ikhale
yopanda chilema. 2 Munthuyo asanjike dzanja lake pamutu pa ng’ombeyo,
ndipo ayiphere pa khomo la tenti ya msonkhano. Ndipo ansembe,
ana a Aaroni, awaze magazi mbali zonse za guwalo. 3 Pa nsembe
yachiyanjanopo, ayenera kupatula zam’kati mwa nyamayo ndi mafuta
onse amene amakuta zam’kati kupereka nsembe ya chakudya kwa
Yehova. 4 Apatulenso impsyo zonse ziwiri pamodzi ndi mafuta ake omwe
ndiponso mafuta okuta chiwindi amene achotsedwa pamodzi ndi impsyo
zija. 5 Ndipo ana a Aaroni atenthe zimenezi pa guwa, pamwamba pa

chopereka chopsereza chimene chili pa nkhuni zoyakazo. Imeneyi ndi
nsembe yotentha pa moto, ya fungo lokomera Yehova.
6 " 'Ngati munthu apereka nsembe ya chiyanjano kwa Yehova, chop-
erekacho chikhale nkhosa yayimuna kapena yayikazi yopanda chilema.
7 Ngati apereka nsembe ya mwana wankhosa, abwere naye pamaso pa
Yehova. 8 Asanjike dzanja lake pamutu pa nkhosayo ndipo ayiphere pa
khomo la tenti ya msonkhano. Ndipo ana a Aaroni awaze magaziwo
mbali zonse za guwalo. 9 Pa nsembe yachiyanjanopo ayenera kuchotsa ndi
kubweretsa: mafuta a nkhosayo, mchira wake wonse wonona atawudulira
m'tsinde pafupi ndi fupa la msana, zam'kati zonse ndi mafuta onse amene
akuta ziwalo zam'katimo, 10 impsyo zonse ziwiri pamodzi ndi mafuta
amene akuta impsyozo, msonga ya chiwindi imene idzachotsedwere
limodzi ndi impsyozo. 11 Wansembe awotche zonsezi pa guwa. Ichi ndi
chakudya chotentha pa moto choperekedwa kwa Yehova.
12 " 'Ngati munthuyo apereka mbuzi ngati nsembe, abwere nayo kwa
Yehova. 13 Asanjike dzanja lake pamutu pa mbuziyo ndipo ayiphere pa
khomo la tenti ya msonkhano. Ndipo ana a Aaroni awaze magazi ake
mbali zonse za guwa. 14 Tsono pa nsembe yoti iwotchedwe kukhala
nsembe chakudya ya Yehova, achotse ndi kubweretsa: mafuta onse amene
amaphimba zam'kati kapena mafuta onse a m'katimo, 15 impsyo zonse
ziwiri pamodzi ndi mafuta onse omwe akuta impsyozo ndi msonga ya
chiwindi imene adzachotsera pamodzi ndi impsyo zija. 16 Wansembe
awotche zonsezi pa guwa. Ichi ndi chakudya cha Yehova, chowotcha pa
moto ndiponso cha fungo lokomera Yehova. Mafuta onse ndi a Yehova.
17 " 'Limeneli likhale lamulo lamuyaya pa mibado yanu yonse kuti
musadzadye mafuta kapena magazi kulikonse kumene mudzakhale.' "

# 4

### *Nsembe Yopepesera Tchimo*

1 Yehova anayankhula ndi Mose kuti, 2 "Awuze Aisraeli kuti, 'Munthu
akachimwa mosadziwa ndi kuchita chilichonse chimene Yehova walamula
kuti asachite, azichita izi:
3 " 'Ngati wansembe wodzozedwa achimwa, ndi kuchimwitsa anthu
onse, iyeyu ayenera kupereka mwana wang'ombe wamphongo wopanda
chilema chifukwa cha tchimo limene wachitalo. Imeneyi ndi nsembe ya
Yehova yopepesera tchimo lake. 4 Wansembeyo abwere nayo ng'ombeyo
pa khomo la tenti ya msonkhano pamaso pa Yehova. Asanjike dzanja
lake pamutu pa ng'ombeyo ndipo ayiphe pamaso pa Yehova. 5 Kenaka
wansembe wodzozedwa atengeko magazi a ng'ombeyo ndi kulowa nawo
mu tenti ya msonkhano. 6 Iye aviyike chala chake m'magazi, ndipo
awawaze kasanu ndi kawiri pamaso pa Yehova, patsogolo pa katani
yotchinga malo wopatulika. 7 Kenaka wansembe apake magaziwo pa
nyanga za guwa lofukizira lubani limene lili pamaso pa Yehova mu tenti ya
msonkhano. Magazi ena otsalawo awathire pa tsinde pa guwa lansembe
zopsereza, limene lili pa khomo la tenti ya msonkhano. 8 Pambuyo pake
achotse mafuta onse a ng'ombe yayimuna yopepesera machimoyo: mafuta
okuta zam'kati kapena mafuta onse am'katimo. 9 Achotsenso ndi kubwera
ndi impsyo zonse ziwiri pamodzi ndi mafuta onse ndiponso mafuta onse
amene aphimba chiwindi ndi impsyo 10 monga momwe amachotsera
mafuta a ng'ombe yoperekedwa kuti ikhale chopereka chachiyanjano.

Tsono wansembe atenthe zimenezi pa guwa lansembe zopsereza. [11] Koma
chikopa cha ng'ombe yayimunayo ndi mnofu wake wonse, pamodzi ndi
mutu ndi miyendo, zam'kati ndi matumbo, [12] kapena kuti ng'ombe yonse
yotsalayo apite nayo kunja kwa msasa ku malo woyeretsedwa, kumene
amatayako phulusa ndi kuyitentha pa nkhuni, pa phulusapo.

[13] " 'Ngati gulu lonse la Aisraeli lichimwa mosadziwa, nachita chomwe
ndi choletsedwa ndi Yehova, ngakhale kuti gulu lonselo silikudziwa kuti
lachimwa, anthuwo ndi olakwa ndithu. [14] Akazindikira tchimo limene
achita, gulu lonse lipereke mwana wang'ombe wamphongo kuti akhale
chopereka chopepesera tchimo ndipo abwere naye pa khomo la tenti ya
msonkhano. [15] Akuluakulu a anthuwo asanjike manja awo pa mutu pa
ng'ombe pamaso pa Yehova, ndipo ayiphe pomwepo pamaso pa Yehova.
[16] Tsono wansembe wodzozedwa atengeko magazi a ng'ombeyo ndi
kulowa nawo mu tenti ya msonkhano. [17] Aviyike chala chake m'magaziwo
ndi kuwawaza pamaso pa Yehova kasanu ndi kawiri patsogolo pa nsalu
yotchinga. [18] Pambuyo pake iye apake magaziwo pa nyanga za guwa
limene lili pamaso pa Yehova mu tenti ya msonkhano. Magazi ena
otsalawo awathire pa tsinde pa guwa lansembe zopsereza limene lili pa
khomo la tenti ya msonkhano. [19] Kenaka achotse mafuta onse a ng'ombeyo
ndi kuwatentha pa guwa, [20] ndipo achite ndi ng'ombe yayimunayi
monga anachitira ndi ng'ombe yayimuna yopepesera machimo. Potero,
wansembe adzapereka nsembe yopepesera anthu, ndipo machimo awo
adzakhululukidwa. [21] Kenaka atulutse ng'ombeyo kunja kwa msasa ndi
kuyitentha monga anatenthera ng'ombe yoyamba ija. Imeneyi ndiyo
nsembe yopepesera machimo a gulu lonse.

[22] " 'Ngati mtsogoleri achimwa mosadziwa nachita zimene ndi zo-
letsedwa ndi Yehova Mulungu wake, ndiye kuti wapalamula. [23] Ndipo
ngati wauzidwa za tchimo limene wachita, iye abwere ndi mbuzi
yayimuna yopanda chilema kuti ikhale chopereka chake. [24] Asanjike
dzanja lake pa mutu wa mbuziyo ndi kuyiphera pamalo pamene amaphera
zopereka zopsereza pamaso pa Yehova. Ichi ndi chopereka chopepesera
tchimo. [25] Pambuyo pake wansembe atengeko magazi a chopereka
chopepesera tchimocho ndi chala chake, ndipo awapake pa nyanga za
guwa lansembe zopsereza. Athire magazi otsalawo pa tsinde la guwalo.
[26] Wansembeyo atenthe mafuta onse pa guwapo monga amatenthera
chopereka chachiyanjano. Pochita zimenezi, wansembe adzapereka
nsembe yopepesera tchimo la munthuyo, ndipo adzakhululukidwa.

[27] " 'Ngati munthu wamba achimwa mosadziwa nachita zimene ndi
zoletsedwa ndi Yehova, ndiye kuti wapalamula. [28] Ndipo ngati wauzidwa
za tchimo limene wachita, abweretse mbuzi yayikazi yopanda chilema kuti
ikhale chopereka chopepesera tchimo. [29] Asanjike dzanja lake pamutu pa
mbuziyo ndipo ayiphe pamalo pamene amaphera chopereka chopsereza.
[30] Ndipo wansembe atenge magazi ndi chala chake ndi kuwapaka pa
nyanga za guwa lansembe zopsereza ndi kuthira magazi wotsalawo pa
tsinde la guwalo. [31] Kenaka iye achotse mafuta onse monga momwe
anachotsera mafuta a chopereka chachiyanjano, ndipo awatenthe pa
guwa kuti akhale fungo lokomera Yehova. Potero, wansembe adzapereka
nsembe yopepesera tchimo la munthuyo ndipo adzakhululukidwa.

[32] " 'Ngati munthu apereka mwana wankhosa ngati chopereka chopepe-
sera tchimo lake, abwere ndi mwana wankhosa wamkazi wopanda
chilema. [33] Asanjike dzanja lake pa mutu wa mwana wankhosayo ndipo

amuphe pamalo pamene amaphera chopereka chopsereza. 34 Kenaka
wansembe atengeko ndi chala chake magazi a mwana wankhosa uja ndi
kuwapaka pa nyanga za guwa lansembe zopsereza. Magazi otsalawo
athire pa tsinde la guwalo. 35 Iye achotse mafuta onse, monga ama-
chotsera mafuta a mwana wankhosa wa chopereka chachiyanjano, ndipo
wansembe awatenthe pa guwa pamodzi ndi zopereka zina zopsereza za
Yehova. Potero, wansembe adzapereka nsembe yopepesera tchimo limene
munthuyo anachita ndipo adzakhululukidwa.

# 5

1 “ ‘Ngati munthu anayitanidwa ku bwalo kuti akachitire umboni pa
zimene anaziona kapena kuzimva koma iye n’kukana kuchitira umboni,
munthu ameneyo wachimwa ndipo ayenera kulangidwa.

2 “ ‘Munthu akakhudza chinthu chilichonse chodetsedwa, monga nyama
yakufa ya m’thengo, kapena chiweto chakufa kapenanso chokwawa chak-
ufa, ngakhale iyeyo wachikhudza mosadziwa, wasanduka wodetsedwa
ndipo wachimwa.

3 “ ‘Munthu akakhudza choyipitsa munthu cha mtundu uliwonse, ndipo
pochikhudzapo ndi kuyipitsidwa nacho mosadziwa, munthuyo adzakhala
wopalamula akangodziwa chimene wachitacho.

4 “ ‘Munthu akalumbira mofulumira kapena mosasamala kuti adzachita
chinthu, choyipa kapena chabwino, ngakhale kuti wachita izi mosadziwa
kuti n’kulakwa, pamene wazindira kulakwa kwake, iye adzakhalabe
wopalamula akangodziwa chimene wachitacho.

5 “ ‘Pamene munthu wazindikira kuti wachimwa motere, awulule
tchimo limene wachitalo. 6 Pambuyo pake, munthuyo abwere kwa Yehova
ndi mwana wankhosa wamkazi kapena mbuzi kuti ikhale chopereka
chopepesera tchimo ndipo wansembe achite mwambo wopepesera tchimo
lomwe wachitalo. Tsono wansembe achite mwambo wopepesera tchimo
la munthuyo.

7 “ ‘Ngati munthuyo alibe mwana wankhosa, abweretse njiwa ziwiri
kapena nkhunda ziwiri kwa Yehova ngati chopereka chopepesera tchimo
lake. Imodzi ikhale nsembe yopepesera tchimo, ndipo inayo ikhale
nsembe yopsereza. 8 Tsono abwere nazo kwa wansembe, ndipo wansem-
beyo ayambe wapereka mbalame imodzi ngati yopepesera tchimo. Apo-
tole khosi koma osayidula mutu, 9 kenaka awaze magazi a chopereka
chopepesera tchimocho m’mbali mwa guwa. Magazi ena onse awathire
pa tsinde la guwa. Imeneyi ndi nsembe yopepesera tchimo. 10 Pambuyo
pake wansembe apereke mbalame inayo kuti ikhale chopereka chopsereza
potsata mwambo wake. Wansembe atatha kupereka nsembe yopepesera
tchimo limene munthu uja wachita, wochimwayo adzakhululukidwa.

11 “ ‘Koma ngati munthuyo alibe njiwa ziwiri kapena nkhunda ziwiri,
abweretse ufa wosalala wokwanira kilogalamu imodzi kuti ukhale chop-
ereka chopepesera tchimo limene wachita. Asathiremo mafuta kapena
lubani chifukwa ndi chopereka chopepesera tchimo. 12 Abweretse ufawo
kwa wansembe ndipo wansembeyo atapeko dzanja limodzi kuti ukhale
ufa wachikumbutso ndi kuwutentha pa guwa pamodzi ndi chopereka
chopsereza kwa Yehova. Imeneyi ndi nsembe yopepesera tchimo. 13 Umu
ndi mmene wansembe adzachitire mwambo wopepesera machimo ena
aliwonse amene munthu wachita, ndipo munthuyo adzakhululukidwa.
Zopereka zonse zotsala zidzakhala za wansembeyo monga momwe
amachitira ndi chopereka chachakudya.’ ”

### *Chopereka Chopepesera Kupalamula*

14 Yehova anawuza Mose kuti, 15 “Munthu akachita zinthu
mosakhulupirika, nachimwa mosadziwa posapereka zinthu zopatulika
zofunika kwa Yehova, munthuyo apereke kwa Yehova nsembe yopepesera
machimo ake. Nsembeyo ikhale nkhosa yayimuna yopanda chilema ndipo
mtengo wake ukhale wokwana masekeli oyenera a siliva pakawerengedwe
ka ku Nyumba ya Mulungu. Imeneyi ndi nsembe yopepesera kupalamula.
16 Munthuyo ayenera kubweza zinthu zopatulika zimene sanaperekezo.
Awonjezepo chimodzi mwa zigawo zisanu zilizonse ndi kuzipereka
zonsezo kwa wansembe amene adzachita mwambo wopepesera machimo
a munthuyo, popereka nkhosa yayimuna ija ngati nsembe yopepesera
ndipo wochimwayo adzakhululukidwa.

17 “Ngati munthu wachimwa mosadziwa pochita chilichonse chimene
Yehova salola, munthuyo ndi wopalamula ndithu, ndipo ayenera ku-
langidwa. 18 Abwere kwa wansembe ndi chopereka chopepesera
kupalamula kwake. Chopereka chikhale nkhosa yayimuna yopanda
chilema ndipo mtengo wake ukhale woyenera nsembe yopepesera ku-
palamula kumene anachimwa mosadziwako, ndipo munthuyo adza-
khululukidwa. 19 Imeneyi ndi nsembe yopepesera kupalamula popeza
munthuyo wapezeka wolakwa pamaso pa Yehova.”

## 6

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 “Ngati munthu wina aliyense achimwa,
nachita zinthu mosakhulupirika kwa Yehova chifukwa cha kunyenga
mnzake pokana kumubwezera zimene anamusungitsa, kapena kumubera
kapenanso kumulanda, 3 kapena ndi kunama kuti sanatole chinthu
chimene chinatayika, kapena kulumbira mwachinyengo pa chinthu chili-
chonse chimene munthu akachita amachimwa nacho, 4 ndi wopalamula
ndithu, ndipo ayenera kubweza zimene anabazo, zimene analanda
mwachinyengozo, zimene anamusungitsazo, zimene anatolazo 5 kapena
zimene analumbira monyengazo. Pa tsiku limene apezeke kuti wa-
palamuladi, iye ayenera kumubwezera mwini wake zinthu zonsezi ndi
kuwonjezerapo chimodzi mwa zigawo zisanu zilizonse. 6 Pambuyo pake
apereke kwa Yehova nsembe yopalamula. Nsembe yake ikhale nkhosa
yayimuna yopanda chilema ndipo mtengo wake wogwirizana ndi nsembe
yopepesera machimo. 7 Kenaka wansembe achite mwambo wopepesera
tchimo la munthuyo pamaso pa Yehova, ndipo adzakhululukidwa chili-
chonse chomwe anachita kuti akhale wopalamula.”

### *Nsembe Yopsereza*

8 Yehova anawuza Mose kuti, 9 “Lamula Aaroni ndi ana ake kuti, ‘Lamulo
la nsembe yopsereza ndi ili: Nsembe yopserezayo izikhala pa moto pa
guwa usiku wonse mpaka mmawa, ndipo moto wa paguwapo uzikhala
ukuyaka nthawi zonse. 10 Tsono wansembe avale mkanjo wake wa
nsalu yofewa ndi yosalala. M’kati avalenso kabudula wofewa, wosalala.
Pambuyo pake atenge phulusa la nyama imene yatenthedwa pa guwa
lansembe paja ndi kulithira pambali pa guwa lomwelo. 11 Akatero avule
zovala zakezo ndi kuvala zovala zina. Kenaka atulutse phulusalo ndi
kukaliyika pa malo woyeretsedwa kunja kwa chithando. 12 Moto wa pa
guwa uzikhala ukuyaka nthawi zonse, usamazime. Mmawa uliwonse
wansembe aziwonjezerapo nkhuni pa motopo ndi kukonza nsembe

yopsereza, ndi kutentha mafuta a nsembe yachiyanjano pamenepo.
13 Moto uzikhala ukuyaka pa guwa nthawi zonse ndipo usazimepo.

*Nsembe Zachakudya*

14 “ ‘Lamulo la nsembe yachakudya ndi ili: ana a Aaroni azibwera
nayo nsembeyo pamaso pa Yehova, patsogolo pa guwa. 15 Wansembe
mmodzi atapeko dzanja limodzi la ufa wosalala wa nsembe yachakudya
ija kuti ukhala ufa wachikumbutso ndi mafuta pamodzi ndi lubani
yense amene ali pa nsembe ya chakudyacho, ndipo azitenthe pa guwa
kuti zilandiridwe ndi Yehova m’malo mwa nsembe yonse kuti zikhale
nsembe ya fungo lokomera Yehova. 16 Aaroni ndi ana ake azidya
zimene zatsala koma azidya zopanda yisiti ku malo wopatulika, ku
bwalo la tenti ya msonkhano. 17 Poziphika asathire yisiti. Ndawapatsa
zotsalazo kuti zikhale gawo lawo la nsembe zanga zopsereza. Zonsezi
ndi zopatulika kwambiri monga nsembe yopepesera tchimo ndiponso
nsembe yopepesera machimo. 18 Mwana aliyense wamwamuna wa Aaroni
azidyako za nsembe zopsereza zopereka kwa Yehova. Ndi gawo lake
lokhazikika la chopereka chopsereza kwa Yehova pa mibado yanu yonse.
Chilichonse chimene chidzakhudza nsembezo chidzakhala chopatulika.’ ”
19 Yehova anawuzanso Mose kuti, 20 “Nsembe imene Aaroni ndi ana ake
ayenera kupereka kwa Yehova pa tsiku limene wansembe akudzozedwa
ndi iyi: ufa wosalala kilogalamu imodzi ngati chopereka chachakudya
cha nthawi zonse. Azipereka theka limodzi mmawa ndipo theka linalo
madzulo. 21 Ipangidwe ndi mafuta pa chiwaya ndipo ubwere nayo
ili yosakaniza bwino, yophikidwa mitandamitanda monga amachitira
ndi nsembe yachakudya. Iphikidwe moti itulutse fungo lokomera
Yehova. 22 Mwana wa fuko la Aaroni amene adzadzozedwe kukhala
wansembe kulowa m’malo mwa Aaroni ndiye amene azidzakonza ndi
kupereka nsembeyi kwa Yehova nthawi zonse monga kunalembedwera.
23 Nsembe iliyonse yachakudya ya wansembe izitenthedwa kwathunthu,
isamadyedwe.”

*Nsembe Yopepesera Tchimo*

24 Yehova anawuza Mose kuti 25 “Uza Aaroni ndi ana ake kuti, ‘Malamulo
a nsembe ya tchimo ndi awa: Nsembeyi iziphedwa pamaso pa Yehova
pa malo pamene mumaphera nsembe yopsereza popeza ndi nsembe
yopatulika. 26 Wansembe amene apereke nsembeyi adyere ku malo
wopatulika ndiye kuti m’bwalo la tenti ya msonkhano. 27 Chilichonse
chimene chidzakhudza nsembeyo chidzakhala chopatulika, ndipo ngati
magazi ake agwera pa chovala, muchape chovalacho pa malo opatulika.
28 M’phika wadothi umene aphikira nyamayo auphwanye. Koma ngati
yaphikidwa mu m’phika wa mkuwa, awukweche ndi kuwutsukuluza
ndi madzi. 29 Munthu wamwamuna aliyense wa m’banja la wansembe
angathe kuyidya popeza nsembeyi ndi yopatulika kwambiri. 30 Koma
nsembe yopepesera tchimo imene magazi ake amabwera nawo mu tenti ya
msonkhano kudzachita mwambo wopepesera tchimo ku malo opatulika
isadyedwe, m’malo mwake itenthedwe.’ ”

## 7

*Nsembe Yopepesera Kupalamula*

1 “ ‘Malamulo a nsembe yopepesera kupalamula imene ndi nsembe
yopatulika kwambiri ndi awa: 2 Nsembe yopepesera machimo iziphedwa

pamalo pomwe amaphera nsembe yopsereza ndipo awaze magazi ake
mbali zonse za guwa. 3 Tsono apereke mafuta ake onse: mchira wamafuta
ndi mafuta amene amakuta matumbo. 4 Aperekenso impsyo ziwiri, mafuta
ake pamodzi ndi mafuta onse amene ali cham'chiwuno, ndiponso mafuta
onse amene aphimba chiwindi. 5 Wansembe azitenthe pa guwa kuti
zikhale nsembe yotentha pa moto, yoperekedwa kwa Yehova. Imeneyi ndi
nsembe yopepesera tchimo lopalamula. 6 Munthu wamwamuna aliyense
wa m'banja la wansembe angathe kudyako nsembeyo koma adyere ku
malo opatulika. Imeneyi ndi nsembe yopatulika kwambiri.

7 " 'Nsembe yopepesera tchimo lopalamula ndi yofanana ndi nsembe
yoperekedwa chifukwa cha tchimo. Ndipo nsembe ziwiri zonsezi zili
ndi lamulo limodzi lokha. Wansembe amene wachita mwambo wa
nsembe yopepesera machimo a kupalamula atenge nyamayo ngati yake.
8 Wansembe wopereka nsembe yopsereza ya munthu wina aliyense,
atenge chikopa cha nsembe yopserezayo kuti chikhale chake. 9 Chopereka
chilichonse cha chakudya chophika mu uvuni kapena chokazinga mu
m'phika kapena mu chiwaya ndi cha wansembe amene wapereka nsem-
bezo. 10 Ndipo chopereka china chilichonse cha chakudya chosakaniza ndi
mafuta kapena chowuma, chikhale cha ana onse a Aaroni ndipo anawo
achigawane mofanana.

### *Nsembe Yachiyanjano*

11 " 'Malamulo a nsembe ya chiyanjano imene munthu angathe ku-
pereka kwa Yehova ndi awa:

12 " 'Ngati munthuyo apereka chifukwa cha kuthokoza, apereke nsem-
beyo pamodzi ndi makeke wopanda yisiti, osakaniza ndi mafuta; tim-
itanda ta buledi wopanda yisiti, topyapyala, topaka mafuta, ndiponso
makeke a ufa wosalala wophikidwa bwino, wosakaniza ndi mafuta.
13 Pamodzi ndi nsembe yachiyanjano yothokozerayo abwerenso ndi
makeke opangidwa ndi yisiti ngati chopereka chake. 14 Munthuyo atenge
mtanda umodzi pa mtanda wa buledi wa mtundu uliwonse kuti ukhale
nsembe yopereka kwa Yehova. Tsono mtanda umenewo ndi wake wa
wansembe amene awaze magazi a nsembe yachiyanjano. 15 Nyama ya
nsembe yachiyanjano yothokozera idyedwe pa tsiku lomwe nsembeyo
yaperekedwa ndipo isatsaleko mpaka mmawa.

16 " 'Koma ngati nsembe yakeyo apereka chifukwa cha lumbiro kapena
mwaufulu, nsembeyo adye tsiku lomwe yaperekedwalo. Koma yotsala
angathe kuyidya mmawa mwake. 17 Ngati nyama ina ya nsembe yatsalabe
mpaka tsiku lachitatu, imeneyo itenthedwe pa moto. 18 Ngati munthu
adya nyama yachiyanjano pa tsiku lachitatu, nsembeyo sidzalandiridwa.
Amene wayipereka nsembeyo Mulungu sadzamulandira ndipo nsembeyo
idzakhala yonyansa pamaso pa Mulungu, yosamupindulira kanthu wop-
erekayo.

19 " 'Nyama imene yakhudza chilichonse chodetsedwa, munthu
asayidye, koma itenthedwe pa moto. Aliyense amene ali woyeretsedwa
angathe kudya nyama inayo. 20 Koma ngati munthu wina amene ndi
wosayeretsedwa adya nyama ya nsembe yachiyanjano imene ndi ya
Yehova, ameneyo achotsedwe pakati pa anthu a mtundu wake. 21 Ndipo
ngati munthu wina akhudza chinthu chodetsedwa, kaya chonyansa cha
munthu kapena cha nyama, kapenanso chonyansa china chilichonse,

ndipo kenaka n'kudya nyama ya nsembe yachiyanjano imene ndi ya
Yehova, munthu ameneyo achotsedwe pakati anthu a mtundu wake.' "

### *Za Kuletsa Kudya Mafuta ndi Magazi*

22 Yehova anayankhula ndi Mose kuti, 23 "Awuze Aisraeli kuti, 'Musadye
mafuta a ng'ombe, nkhosa kapenanso mbuzi. 24 Mafuta a nyama
yofa yokha, kapena mafuta a nyama yophedwa ndi zirombo akhoza
kuwagwiritsa ntchito iliyonse, koma inu musadye mafuta amenewo.
25 Pakuti munthu wakudya mafuta a nyama yoperekedwa kwa Yehova
ngati nsembe yotentha pa moto, ayenera kuchotsedwa pakati pa anthu a
mtundu wake. 26 Ndipo kulikonse kumene mukakhale musakadye magazi
a mbalame iliyonse kapena magazi a nyama iliyonse. 27 Ngati munthu
aliyense adya magazi achotsedwe pakati pa anthu a mtundu wake.' "

### *Gawo la Ansembe*

28 Yehova anayankhula ndi Mose kuti, 29 "Awuze Aisraeli kuti, Aliyense
amene apereka nsembe yachiyanjano kwa Yehova, abwere ndi gawo la
nsembeyo kwa Yehova. 30 Atenge ndi manja ake zigawo za chopereka
zoyenera kuzitentha pa moto ngati chopereka kwa Yehova. Abweretse
mafuta, pamodzi ndi chidale chomwe, ndipo chidalecho achiweyule
kuti chikhale chopereka choweyula kwa Yehova. 31 Wansembe atenthe
mafutawo pa guwa koma chidalecho chikhale cha Aaroni ndi ana ake.
32 Mumupatse wansembe ntchafu ya kumanja ya nsembe yanu yachiyan-
jano kuti ikhale chopereka chanu kwa iye. 33 Mwana wa Aaroni amene
amapereka magazi ndi mafuta a nsembe yachiyanjano, adzitenga ntchafu
ya kumanja kukhala gawo lake. 34 Choncho pa zopereka zachiyanjano za
Aisraeli, Ine ndatengapo chidale chomwe amaweyula ndi ntchafu zimene
amapereka nsembe ndipo ndazipereka kwa wansembe Aaroni ndi ana
ake. Izi ndizo gawo lawo nthawi zonse pa zopereka za Aisraeli."

35 Zimenezi ndi chigawo cha Aaroni ndi ana ake chotapidwa pa zopereka
kwa Yehova zoti zitenthedwe pa moto zimene zinaperekedwa pa tsiku
limene anapatulidwa kuti akhale ansembe otumikira Yehova. 36 Yehova
ndiye analamulira kuti pa zopereka za Aisraeli azitapapo zimenezi ndi
kuwapatsa ansembe ngati gawo lawo. Yehovayo analamula zimenezi
pa tsiku limene ansembewo anapatulidwa ndipo anachikhazikitsa ngati
lamulo la nthawi zonse.

37 Awa ndi malamulo a nsembe izi: nsembe yopsereza, nsembe
yachakudya, nsembe yopepesera machimo, nsembe yopepesera ku-
palamula, nsembe ya mwambo wodzoza ndi nsembe yachiyanjano.
38 Malamulo amenewa Yehova anapereka kwa Mose pa Phiri la Sinai pa
tsiku limene Yehova analamulira Aisraeli kuti abwere ndi zopereka za kwa
Yehova, ku chipululu cha Sinai kuja.

## 8

### *Mwambo Wodzoza Aaroni ndi Ana Ake*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Tenga Aaroni ndi ana ake, zovala zawo,
mafuta wodzozera, ng'ombe yayimuna kuti ikhale nsembe yopepesera
machimo, nkhosa ziwiri zazimuna ndi dengu la buledi wopanda yisiti,
3 ndipo usonkhanitse gulu la anthu pa khomo la tenti ya msonkhano."
4 Mose anachita zomwe Yehova anamulamula ndipo gulu la anthu
linasonkhana pa khomo la tenti ya msonkhano.

5 Mose anawuza gulu la anthuwo kuti, “Izi ndi zimene Yehova wala-
mulira kuti zichitike.” 6 Pamenepo Mose anabwera ndi Aaroni ndi ana ake
nawasambitsa ndi madzi. 7 Anamuveka Aaroni mwinjiro, ndi kumumanga
lamba m’chiwuno. Anamuvekanso mkanjo wa efodi ndi efodiyo. Ana-
mangira lamba efodiyo amene analukidwa mwaluso uja, motero efodiyo
analimba m’chiwunomo. 8 Anamuvekanso chovala chapachifuwa ndipo
m’chovalacho anayikamo Urimu ndi Tumimu. 9 Kenaka anamuveka
Aaroniyo nduwira kumutu ndipo patsogolo pa nduwirayo anayikapo duwa
lagolide, chizindikiro chopatulika monga momwe Yehova analamulira
Mose.

10 Pamenepo Mose anatenga mafuta wodzozera nadzoza tenti ya
msonkhano pamodzi ndi zonse zimene zinali m’menemo, ndipo potero
anazipatula. 11 Anawaza mafuta ena pa guwa kasanu ndi kawiri, nalidzoza
guwalo pamodzi ndi ziwiya zake zonse. Anadzozanso beseni ndi tsinde
lake, nazipatula. 12 Anathira mafuta wodzozera ena pamutu pa Aaroni
ndipo anamudzoza ndi kumupatula. 13 Kenaka anabwera ndi ana a
Aaroni. Anawaveka minjiro, ndi kuwamanga malamba m’chiwuno ndi
kuwaveka nduwira kumutu monga momwe Yehova analamulira Mose.

14 Kenaka Mose anabwera ndi ng’ombe yayimuna ya nsembe yopepesera
machimo, ndipo Aaroni ndi ana ake anasanjika manja awo pamutu
pa ng’ombeyo. 15 Mose anapha ng’ombeyo, ndi kutenga magazi ena
ang’ombeyo ndi kupaka ndi chala chake pa nyanga zaguwa lansembe,
naliyeretsa. Magazi otsalawo anawakhuthulira pa tsinde laguwalo.
Motero anachita mwambo wopepesera machimo. 16 Mose anatenganso
mafuta onse okuta matumbo, mafuta ophimba chiwindi, ndiponso impsyo
zonse ziwiri pamodzi ndi mafuta ake, nazitentha pa guwapo. 17 Koma
nyama yang’ombeyo, chikopa chake ndi matumbo ake anaziwotcha kunja
kwa msasa monga momwe Yehova analamulira Mose.

18 Kenaka anabwera ndi nkhosa yayimuna ya nsembe yopsereza, ndipo
Aaroni ndi ana ake aamuna anasanjika manja awo pamutu pake. 19 Ndipo
Mose anapha nkhosayo ndi kuwaza magazi ake mbali zonse zaguwalo.
20 Anayidula nkhosayo nthulinthuli ndipo anatentha mutu wake, nthulizo
ndi mafuta. 21 Anatsuka matumbo ake ndi miyendo yake, ndi kutentha
nkhosa yonseyo pa guwa lansembe kuti ikhale nsembe yopsereza, fungo
lokoma, nsembe yachakudya yoperekedwa kwa Yehova monga Yehovayo
analamulira Mose.

22 Kenaka Mose anapereka nkhosa yayimuna ina pamwambo wodzoza
ansembe, ndipo Aaroni ndi ana ake aamuna anasanjika manja awo
pamutu pake. 23 Mose anayipha nkhosayo ndipo anatenga magazi ake ena
ndi kupaka ndewere za khutu la kudzanja lamanja la Aaroni, pa chala
chake chachikulu cha kudzanja lamanja, ndi pa chala chake chachikulu
cha phazi lakumanja. 24 Pambuyo pake Mose anabwera ndi ana aamuna
a Aaroni ndi kupaka magazi pa ndewere za makutu awo akumanja, pa
zala zawo zazikulu za dzanja lamanja, ndiponso pa zala zawo zazikulu za
kuphazi lakumanja. Kenaka iye anawaza magazi otsalawo mbali zonse za
guwalo. 25 Anatenganso mafuta ake, mafuta a ku mchira wake, mafuta
okuta matumbo, mafuta okuta chiwindi, impsyo zonse ziwiri ndi mafuta
ake ndiponso ntchafu yakumanja. 26 Ndipo m’dengu la buledi wopanda
yisiti limene linali pamaso pa Yehova, anatengamo buledi mmodzi, buledi
mmodzi wokhala ndi mafuta a olivi, ndi buledi wopyapyala mmodzi.
Zonsezi anaziyika pa mafuta aja ndi pa ntchafu ya ku dzanja lamanja

ija. 27 Mose anapereka zonsezi m'manja mwa Aaroni ndi ana ake amene
anazipereka kwa Yehova kuti zikhale nsembe yoweyula. 28 Kenaka
Mose anazitenga m'manja mwawo ndipo anazipsereza pa guwa lansembe
pamwamba penipeni pamodzi ndi nsembe yopsereza ija kuti ikhale
nsembe yopereka pamwambo wodzoza ansembe, kuti ipereke fungo
lokoma, chopereka chachakudya kwa Yehova. 29 Mose anatenga chidale
cha nkhosa yayimuna, chomwe ndi gawo lake pamwambo wodzoza
ansembe, ndipo anachiweyula pamaso pa Yehova kuti chikhale nsembe
yoweyula monga momwe Yehova analamulira Mose.

30 Kenaka Mose anatenga mafuta wodzozera ansembe ndi magazi amene
anali pa guwa nawaza pa Aaroni ndi zovala zake ndiponso ana ake aja ndi
zovala zawo. Motero Mose anapatula Aaroni ndi zovala zake, ndiponso
ana ake ndi zovala zawo.

31 Mose anawuza Aaroni ndi ana ake kuti, “Phikani nyamayo pa khomo
la tenti ya msonkhano, ndipo mudyere pomwepo pamodzi ndi buledi
amene ali m'dengu la zopereka za pamwambo wodzoza ansembe monga
Yehova analamulira kuti, ‘Aaroni ndi ana ake azidya zimenezi.’ 32 Ndipo
nyama ndi buledi zotsalazo, muziwotche. 33 Musatuluke kunja kwa tenti
ya msonkhano kwa masiku asanu ndi awiri mpaka masiku amwambo
wokudzozani unsembe atatha, pakuti mwambowu ndi wa masiku asanu
ndi awiri. 34 Zimene zachitika lerozi analamula ndi Yehova kuti zichitike
ngati nsembe yopepesera machimo anu. 35 Muzikhala pa khomo la tenti ya
msonkhano usana ndi usiku kwa masiku asanu ndi awiri. Ndipo muzichita
zimene Yehova wakulamulani kuti musafe, pakuti zimenezi ndi zomwe
Yehova wandilamulira.” 36 Choncho Aaroni ndi ana ake anachita zonse
zimene Yehova analamula kudzera mwa Mose.

# 9

*Ansembe Ayamba Kutumikira*

1 Pa tsiku lachisanu ndi chitatu Mose anayitana Aaroni, ana ake ndi
akuluakulu a Aisraeli. 2 Ndipo anawuza Aaroni kuti, “Tenga mwana
wang'ombe wamwamuna kuti akhale nsembe yako yopepesera machimo
ndi nkhosa yayimuna kuti ikhale nsembe yopsereza. Zonsezi zikhale
zopanda chilema ndipo uzipereke pamaso pa Yehova. 3 Kenaka uwawuze
Aisraeli kuti, ‘Tengani mbuzi yayimuna kuti ikhale nsembe yopepesera
machimo. Mutengenso mwana wang'ombe ndi mwana wankhosa. Zon-
sezi zikhale za chaka chimodzi ndi zopanda chilema kuti zikhale nsembe
yopsereza. 4 Mutengenso ng'ombe yayimuna ndi nkhosa yayimuna
kuti zikhale nsembe yachiyanjano zoti ziperekedwe pamaso pa Yehova.
Pamodzi ndi izi mubwerenso ndi nsembe yachakudya yosakaniza ndi
mafuta pakuti lero Yehova akuonekerani.’ ”

5 Anthu anatenga zonse zimene Mose analamula nabwera nazo pa
khomo la tenti ya msonkhano. Gululo linasendera pafupi ndi kuyima
pamaso pa Yehova. 6 Tsono Mose anati, “Izi ndi zimene Yehova walamula
kuti muchite kuti ulemerero wa Yehova ukuonekereni.”

7 Pambuyo pake Mose anawuza Aaroni kuti, “Sendera pafupi ndi guwa
ndipo upereka nsembe yako yopepesera machimo ndi nsembe yako
yopsereza ndikuchita mwambo wopepesera machimo ako ndi machimo
a anthu. Anthuwa apereke nsembe zawo zopepesera machimo monga
momwe Yehova walamulira.”

8 Choncho Aaroni anasendera pafupi ndi guwa, napha mwana
wang'ombe uja kukhala nsembe yake yopepesera machimo. 9 Ana a

Aaroni anabwera ndi magazi kwa Aaroni ndipo iye anaviyika chala
chake m'magaziwo, nawapaka pa nyanga za guwa. Magazi wotsalawo
anawathira pa tsinde la guwalo. 10 Kenaka anatentha paguwapo,
mafuta, impsyo pamodzi ndi mafuta amene amakuta chiwindi ngati
nsembe yopepesera machimoyo, monga momwe Yehova analamulira
Mose. 11 Koma nyama ndi chikopa anazitenthera kunja kwa msasa.

12 Kenaka anapha nsembe yopsereza. Ana a Aaroni atabwera ndi
magazi kwa iye, Aaroniyo anawawaza mbali zonse za guwa. 13 Ana
akewo anamupatsa nyama yoduladula ya nsembe yopsereza ija pamodzi
ndi mutu ndipo anazitentha pa guwa. 14 Aaroni anatsuka matumbo ndi
miyendo nazitentha pa guwa pamodzi ndi nsembe yopsereza ija.

15 Kenaka Aaroni anapereka zopereka za anthuwo. Anatenga mbuzi
yopepesera machimo a anthuwo, yopereka chifukwa cha tchimo, nayipha
ndi kuyipereka kuti ikhale yopepesera machimo monga anachitira ndi
nsembe yoyamba ija.

16 Anabwera ndi nsembe yopsereza, nayipereka potsata mwambo wake.
17 Anabweranso ndi chopereka cha chakudya. Anatapa ufa dzanja limodzi
ndi kutentha pa guwa, kuwonjezera pa nsembe yopsereza ya mmawa ija.

18 Tsono Aaroni anapha ng'ombe ndi nkhosa yayimuna monga nsembe
yachiyanjano ya anthu. Ana ake anamupatsira magazi ndipo anawawaza
mbali zonse za guwa. 19 Anamupatsiranso mafuta a ng'ombeyo ndi nkhosa
yayimunayo: mchira wamafuta, mafuta wokuta matumbo, impsyo ndi
mafuta wokuta chiwindi. 20 Ana a Aaroni anayika mafutawo pa zidale.
Pambuyo pake Aaroni anatentha mafutawo pa guwa lansembe. 21 Koma
zidale ndi ntchafu ya kumanja Aaroni anaziweyula ngati chopereka
choweyula pamaso pa Yehova.

22 Kenaka Aaroni anakweza manja ake pa anthuwo nawadalitsa. Ndipo
atatha kupereka nsembe yopepesera machimo, nsembe yopsereza ndi
nsembe yachiyanjano, anatsika pa guwapo.

23 Ndipo Mose pamodzi ndi Aaroni analowa mu tenti ya msonkhano.
Atatulukamo anadalitsa anthuwo ndipo ulemerero wa Yehova unaonekera
kwa anthu onse. 24 Pomwepo moto unatuluka pamaso pa Yehova
niwutentha nsembe zopsereza ndi mafuta zimene zinali pa guwa. Anthu
onse ataona zimenezi anafuwula mwachimwemwe ndipo anaweramitsa
nkhope zawo pansi.

# 10

*Imfa ya Nadabu ndi Abihu*

1 Ana a Aaroni, Nadabu ndi Abihu, aliyense anatenga chofukizira lubani
chake nayikamo makala a moto ndi kuthiramo lubani. Iwo anapereka
pamaso pa Yehova moto wachilendo, moto umene Yehova sanawalamule.
2 Choncho moto unatuluka pamaso pa Yehova ndi kuwapsereza, ndipo
anafa pamaso pa Yehova. 3 Pamenepo Mose anawuza Aaroni kuti, "Pajatu
Yehova ananena kuti,

" 'Kwa iwo amene amandiyandikira
ndidzaonetsa ulemerero wanga;
pamaso pa anthu onse
ndidzalemekezedwa.' "

Aaroni anakhala chete wosayankhula.

4 Mose anayitana Misaeli ndi Elizafani, ana a Uzieli, abambo ang'ono a
Aaroni, ndipo anawawuza kuti, "Bwerani kuno mudzachotse abale anuwa

pa malo wopatulika ndi kuwatulutsira kunja kwa msasa.” 5 Choncho
anabwera atavala minjiro yawo ndipo anawatenga ndi kuwatulutsa kunja
kwa msasawo monga momwe Mose analamulira.

6 Ndipo Mose anawuza Aaroni ndi ana ake Eliezara ndi Itamara kuti,
“Musalileke tsitsi lanu nyankhalala ndipo musang’ambe zovala zanu kuti
mungafe, ndi mkwiyo wa Yehova ungagwere anthu onsewa. Koma
abale anu okha, kutanthauza fuko lonse la Israeli ndiwo ayenera kulira
omwalira aja amene Yehova wawapsereza ndi moto. 7 Musatuluke
kunja kwa tenti ya msonkhano, mungafe, chifukwa munadzozedwa ndi
mafuta a Yehova kukhala ansembe.” Choncho iwo anachita monga Mose
ananenera.

8 Pambuyo pake Yehova anayankhula ndi Aaroni nati, 9 “Iwe ndi ana ako
musamamwe vinyo kapena chakumwa chilichonse choledzeretsa pamene
mukulowa mu tenti ya msonkhano kuti mungafe. Ili ndi lamulo lamuyaya
pa mibado yanu yonse. 10 Muzisiyanitsa pakati pa zinthu zopatulika ndi
zinthu wamba, pakati pa zinthu zodetsedwa ndi zinthu zoyeretsedwa,
11 ndipo muyenera kuphunzitsa Aisraeli onse malamulo amene Yehova
wakupatsani kudzera mwa Mose.”

12 Mose anawuza Aaroni ndi ana ake otsalawo, Eliezara ndi Itamara
kuti, “Tengani zopereka zachakudya zopanda yisiti zimene zatsala pa
nsembe zopsereza za kwa Yehova ndipo muzidye pafupi ndi guwa pakuti
ndi zopatulika kwambiri. 13 Muzidye pa malo wopatulika chifukwa
zimenezi ndi gawo lako ndi la ana ako pa zopereka zopsereza kwa Yehova.
Izitu ndi zimene Yehova anandilamulira. 14 Koma iwe pamodzi ndi ana
ako aamuna ndi aakazi muzidya chidale chimene chinaweyulidwa ndi
ntchafu zimene zinaperekedwa nsembe. Muzidye pamalo woyeretsedwa.
Zimenezi zaperekedwa kwa iwe ndi ana ako monga gawo lanu pa
zopereka zachiyanjano zimene apereka Aisraeli. 15 Ntchafu imene
inaperekedwayo ndi chidale chomwe chinaweyulidwacho abwere nazo
pamodzi ndi nsembe ya mafuta ya Yehova yotentha pa moto, ndipo
uziweyule kuti zikhale zopereka zoweyula pamaso pa Yehova. Zimenezi
zizikhala zako ndi ana ako nthawi zonse monga walamulira Yehova.”

16 Pambuyo pake Mose anafunafuna mbuzi ya nsembe yopepesera
machimo koma anapeza kuti anayitentha kale. Apa Mose anakalipira
Eliezara ndi Itamara, ana a Aaroni otsala aja nati, 17 “Chifukwa chiyani
simunadyere pamalo wopatulika nsembe yopepesera machimo ija? Kodi
imene ija siyopatulika? Kodi Yehova sanapereke nyamayo kwa inu kuti
muchotse machimo a mpingo wonse powachitira mwambo wa nsembe
yopepesera machimo pamaso pa Yehova? 18 Pakuti magazi ake sanalowe
nawo ku Malo Wopatulika, mukanadya nyama ya mbuziyo pa malo
wopatulikawo monga Yehova analamulira.”

19 Aaroni anamuyankha Mose kuti, “Lero anthu apereka nsembe
yawo yopepesera machimo ndiponso nsembe yawo yopsereza pamaso pa
Yehova komabe zinthu zoterezi zandichitikira. Kodi Yehova akanakondwa
ndikanadya nsembe yopepesera machimo lero?” 20 Pamene Mose anamva
zimenezi, anakhutira.

# 11

*Chakudya Choyeretsedwa ndi Chodetsedwa*

1 Yehova anayankhula ndi Mose ndi Aaroni kuti, 2 “Awuze Aisraeli kuti,
‘Nyama zomwe mukhoza kudya mwa nyama zonse za dziko lapansi ndi

izi: 3 Nyama iliyonse imene ili ndi chipondero chogawikana pakati ndi
yobzikula mukhoza kudya.
4 “ ‘Koma pali nyama zina zimene zimabzikula kokha kapena ndi
zogawikana zipondero zimene simukuyenera kudya. Nyama zimenezi ndi
ngamira, ngakhale imabzikula ilibe zipondero zogawikana. Choncho ndi
yodetsedwa, musadye. 5 Ina ndi mbira, ngakhale imabzikula, zipondero
zake n’zosagawikana. Choncho ndi yodetsedwa, musadye. 6 Inanso ndi
kalulu, ngakhale amabzikula, zipondero zake n’zosagawikana. Choncho
ndi wodetsedwa, musadye. 7 Nkhumba simabzikula ngakhale ili ndi
zipondero zogawikana. Choncho ndi yodetsedwa, musadye. 8 Musamadye
nyama yake kapena kukhudza imene yafa chifukwa ndi yodetsedwa.
9 “ ‘Mwa zamoyo zonse zimene zimakhala m’madzi a m’nyanja ndi
a m’mitsinje mukhoza kudya chilichonse chimene chili ndi minga ya
pa msana ndi mamba. 10 Koma zamoyo zonse za m’nyanja kapena
za m’mitsinje zimene zilibe minga ya pa msana ndi mamba, kaya ndi
tizirombo tonse ta m’madzi ndi zamoyo zonse zopezeka m’menemo ndi
zodetsedwa kwa inu. 11 Pakuti zimenezi ndi zodetsedwa kwa inu, nyama
yake musadye, ndipo zikafa zikhalebe zodetsedwa kwa inu. 12 Chamoyo
chilichonse cha m’madzi chimene chilibe minga ya pa msana kapena
mamba ndi chodetsedwa kwa inu.
13 “ ‘Mbalame zimene simukuyenera kudya chifukwa ndi zodetsedwa
ndi izi: mphungu, nkhwazi, mwimba, 14 nankapakapa, akamtema a
mitundu yonse, 15 akhungubwi a mitundu yonse, 16 kadzidzi wamphondo,
kadzidzi wodzuma, chipudo ndi mtundu uliwonse wa akabawi 17 kadzidzi
wamng’ono, chiswankhono ndi mantchichi, 18 tsekwe, vuwo, dembo,
19 indwa, zimeza za mitundu yonse, nsadzu ndi mleme.
20 “ ‘Zowuluka zonse za miyendo inayi ndi zodetsedwa. 21 Komabe mwa
zowuluka zokhala ndi miyendo inayi zimene mukhoza kudya ndi zokhazo
zimene zili ndi miyendo yolumphira. 22 Pa zimenezo mungathe kudya izi:
dzombe la mitundu yonse, atsokonombwe a mitundu yonse, nkhululu za
mitundu yonse, ndi ziwala za mitundu yonse. 23 Koma za mapiko zina
zonse zokhala ndi miyendo inayi muzitenge kukhala zodetsedwa kwa inu.
24 “ ‘Zimenezi zidzakudetsani. Aliyense wozikhudza zitafa adzakhala
wodetsedwa mpaka madzulo. 25 Aliyense wonyamula chiwalo chilichonse
cha nyama zakufazo ayenera kuchapa zovala zake, ndipo adzakhala
wodetsedwa mpaka madzulo.
26 “ ‘Nyama iliyonse imene ili ndi ziboda zogawikana koma mapazi
ake wosagawikana, kapena imene sibzikula muyiyese yodetsedwa kwa
inu ndipo munthu aliyense akakhudza nyama yakufayo, adzakhala
wodetsedwa. 27 Mwa nyama zonse zoyenda ndi miyendo inayi, nyama
zonse zokhala ndi zikhadabo kuphazi muzitenge kukhala zodetsedwa
ndipo aliyense wozikhudza zitafa adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo.
28 Aliyense wonyamula nyamazi zitafa ayenera kuchapa zovala zake,
ndipo adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo. Zimenezi ndi zodetsedwa
kwa inu.
29 “ ‘Mwa nyama zokwawa, zimene zili zodetsedwa kwa inu ndi izi:
likongwe, mbewa, msambulu za mitundu yonse, 30 gondwa, mng’azi,
buluzi, dududu ndi nanzikambe. 31 Mwa nyama zonse zoyenda pansi,
zimenezi ndi zodetsedwa kwa inu. Munthu aliyense wozikhudza
zitafa adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo. 32 Iliyonse mwa nyama
zimenezi ikafa ndi kugwera pa chiwiya chilichonse, kaya chimagwira

ntchito yotani, kaya ndi chopangidwa ndi mtengo, kaya ndi cha
nsalu, kaya ndi cha chikopa kapena chiguduli chiwiyacho chidzakhala
chodetsedwa. Muchiviyike m'madzi chiwiyacho komabe chidzakhala
chodetsedwa mpaka madzulo, ndipo kenaka chidzakhala choyeretsedwa.
33 Tsono nyama ina iliyonse mwa zimenezi ikagwera m'mbiya ya dothi,
ndiye kuti chilichonse cha m'mbiyamo chidzakhala chodetsedwa, ndipo
muyenera kuswa mbiyayo. 34 Chakudya chilichonse chimene mungadye
chikakhala kuti chathiridwa m'mbiyamo, ndiye kuti chakudyacho chidza-
khala chodetsedwa, ndipo madzi akumwa wochokera m'mbiya zotere
ndi wodetsedwa. 35 Chiwalo chilichonse cha nyama yakufa chikagw-
era pa chinthu chilichonse kaya pa uvuni, kapena pa m'phika, ndiye
kuti zinthuzo zidzakhala zodetsedwa, ndipo ziphwanyidwe popeza ndi
zodetsedwa. 36 Koma kasupe kapena chitsime chamadzi chidzakhala
choyeretsedwa ngakhale kuti chilichonse chokhudza nyama yakufayo
chidzakhala chodetsedwa. Zimenezi muzitenge kukhala zodetsedwa.
37 Chiwalo chilichonse cha nyama yakufayo chikagwera pa mbewu zimene
akuti adzale, mbewu zimenezo zidzakhalabe zabwino. 38 Koma mbewuzo
zikakhala zonyowa ndi madzi, ndipo chiwalo chilichonse cha nyama
zakufazo chikagwera pa mbewuzo, mbewuzo zikhale zodetsedwa kwa inu.

39 " 'Ngati nyama imene mumaloledwa kudya yafa yokha, ndiye
kuti aliyense wokhudza nyama yakufayo adzakhala wodetsedwa mpaka
madzulo. 40 Aliyense amene adyako nyama yakufayo achape zovala zake,
ndipo adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo. Aliyense amene wanya-
mula nyama yakufayo ayenera kuchapa zovala zake, ndipo adzakhala
wodetsedwa mpaka madzulo.

41 " 'Chinthu chilichonse chokwawa pansi ndi chonyansa, simuyenera
kudya. 42 Musadye chilichonse chokwawa pansi, choyenda chamimba
kapena choyenda ndi miyendo inayi kapenanso yambiri popeza ndi
chodetsedwa. 43 Musadzisandutse nokha odetsedwa ndi chokwawa
chilichonse. Musadziyipitse nazo, kuti mukhale odetsedwa. 44 Ine
ndine Yehova Mulungu wanu, choncho dziyeretseni kuti mukhale woyera,
chifukwa Ine ndine woyera. Musadzisandutse odetsedwa ndi chokwawa
chilichonse. 45 Ine ndine Yehova amene ndinakutulutsani ku Igupto kuti
ndikhale Mulungu wanu. Tsono mukhale woyera, chifukwa Ine ndine
woyera.

46 " 'Amenewa ndi malamulo onena za nyama, mbalame, chamoyo
chilichonse choyenda m'madzi ndiponso chamoyo chilichonse chokwawa.
47 Muzisiyanitsa pakati pa chodetsedwa ndi choyeretsedwa, komanso
pakati pa zomwe mutha kudya ndi zomwe simuyenera kudya.' "

## 12

### *Kudziyeretsa kwa Mkazi Atabala Mwana*

1 Yehova anayankhula ndi Mose kuti, 2 "Awuze Aisraeli kuti, 'Mkazi
akakhala woyembekezera, nabala mwana wa mwamuna, mkaziyo adza-
khala wodetsedwa kwa masiku asanu ndi awiri, ngati pa masiku ake
akusamba. 3 Pa tsiku lachisanu ndi chitatu, mwanayo achite mdulidwe.
4 Mkaziyo adikire masiku ena 33 kuti ayeretsedwe ku matenda ake.
Asakhudze kanthu kalikonse koyera kapena kulowa m'malo wopatulika
mpaka masiku a kuyeretsedwa kwake atatha. 5 Ngati abala mwana
wamkazi, adzakhala wodetsedwa kwa masabata awiri, monga zikhalira

pa nthawi yake yosamba. Ndipo mkaziyo adikire masiku ena 66, kuti ayeretsedwe ku matenda akewo.
6 " 'Masiku ake wodziyeretsa akatha, kaya ndi a mwana wamwamuna kapena a mwana wamkazi, abwere kwa wansembe ndi mwana wankhosa wa chaka chimodzi pa khomo la tenti ya msonkhano kuti ikhale nsembe yopsereza. Abwerenso ndi chiwunda cha nkhunda kapena njiwa kuti
ikhale nsembe yopepesera machimo. 7 Wansembeyo apereke zimenezi
pamaso pa Yehova pochita mwambo wopepesera mkaziyo. Ndipo mkaziyo adzakhala woyeretsedwa ku msambo wake.
" 'Amenewa ndiwo malamulo a mkazi amene wabala mwana wamwa-
muna kapena wamkazi. 8 Ngati mkaziyo sangathe kupeza mwana
wankhosa, abwere ndi njiwa ziwiri kapena mawunda ankhunda awiri: imodzi ikhale ya nsembe yopsereza ndipo inayo ikhale ya nsembe yopepesera machimo. Tsono wansembe achite mwambo wopepesera wa mkaziyo ndipo adzayeretsedwa.' "

# 13

## *Malamulo a Nthenda za pa Khungu Zopatsirana*

1 Yehova anawuza Mose ndi Aaroni kuti, 2 "Munthu akakhala ndi
chithupsa, kapena m'buko, kapena chikanga pa thupi lake chimene chitha kusanduka nthenda ya khate, abwere naye munthuyo kwa Aaroni wansembe kapena kwa mmodzi mwa ana ake amene ndi ansembe.
3 Tsono wansembe ayang'anitsitse nthendayo pa khungupo, ndipo ngati
ubweya wa pamalo pamene pali nthendapo wasanduka woyera, komanso kuti nthendayo yazama m'kati kupitirira khungu, ndiye kuti nthendayo ndi khate. Wansembe akamuonetsetsa alengeze kuti ndi wodetsedwa.
4 Ngati chikanga cha pa khungulo chikuoneka choyera, ndipo kuya kwake
sikukuonekera kuti kwapitirira khungu ndi ubweya wake pamalopo sunasanduke woyera, wansembe amuyike wodwalayo padera kwa masiku
asanu ndi awiri. 5 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri wansembe amuonenso
bwino wodwalayo. Ndipo ngati waona kuti nthendayo sinasinthe ndipo sinafalikire pa khungu, amuyikenso wodwalayo padera kwa masiku
ena asanu ndi awiri. 6 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri wansembeyo
amuonenso bwino munthuyo, ndipo ngati nthendayo yazima ndi kusafa-likira pa khungu, wansembe amutchule munthuyo kuti ndi woyera. Umenewo unali m'buko chabe. Choncho munthuyo achape zovala zake
ndipo adzakhala woyera. 7 Koma ngati m'bukowo ufalikira pakhungu
atakadzionetsa kale kwa wansembe ndipo wansembeyo n'kulengeza kuti munthuyo ndi woyeretsedwa, ndiye kuti apitenso kukadzionetsa kwa
wansembeyo. 8 Wansembe amuonetsetsenso munthuyo, ndipo ngati
m'bukowo wafalikira pa khungu, wansembe alengeze kuti munthuyo ndi wodetsedwa ndi kuti nthendayo ndi khate.
9 "Ngati munthu aliyense ali ndi nthenda ya pakhungu yoyipitsa thupi,
wodwalayo abwere naye kwa wansembe. 10 Wansembe amuonetsetse
munthuyo, ndipo ngati ali ndi chithupsa chamaonekedwe woyera pa khungupo chimene chasandutsa ubweya wa pamalopo kukhala woyera,
ndipo ngati pali zilonda pa chotupacho, 11 limenelo ndi khate lachikhalire
la pa khungu, ndipo wansembe alengeze kuti munthuyo ndi wodetsedwa. Asamutsekere munthu woteroyo pakuti ndi wodetsedwa kale.
12 "Ndipo ngati, m'kuona kwa wansembe, khate lija lafalikira pa khungu
lonse moti lamugwira thupi lonse kuyambira kumutu mpaka kumapazi,
13 wansembe amuonetsetse munthuyo, ndipo ngati khatero lagwira thupi

lake lonse, wansembe alengeze kuti munthuyo ndi woyera. Popeza kuti
thupi lonse lasanduka loyera, munthuyo ndi woyeretsedwa. 14 Koma pa
tsiku limene zilonda zidzaoneka pa iye, munthuyo adzakhala wodetsedwa.
15 Wansembe aonetsetse zilondazo ndipo alengeze kuti munthuyo ndi
wodetsedwa. Zilondazo ndi zodetsedwa ndipo ili ndi khate. 16 Koma
zilondazo zikasinthika ndi kusanduka zoyera, munthuyo ayenera kupita
kwa wansembe. 17 Wansembe amuonetsetse ndipo ngati zilondazo
zasanduka zoyera, wansembe amutchule wodwalayo kuti ndi woyera
ndipo adzakhala woyera ndithu.

18 "Ngati pa khungu la munthu wodwalayo pali chithupsa chimene
chinapola kale, 19 ndipo pamalo pamene panali chithupsacho pakatuluka
chotupa choyera kapena banga loyera mofiirira, munthuyo ayenera
kukadzionetsa kwa wansembe. 20 Wansembe aonetsetse bwino ndipo
ngati chikuoneka kuti chazama, ndipo ubweya wa pamalopo wasanduka
woyera, wansembe alengeze kuti munthuyo ndi wodetsedwa. Imeneyo
ndi nthenda ya khate imene yatuluka m'chithupsacho. 21 Koma ngati
wansembe waonetsetsa napeza kuti palibe ubweya woyera ndipo chithup-
sacho sichinazame, koma chazimirira, wansembeyo amuyike padera
wodwalayo kwa masiku asanu ndi awiri. 22 Ngati nthendayo ikufalikira
pa khungu, wansembe alengeze kuti munthuyo ndi wodetsedwa. Limeneli
ndi khate. 23 Koma bangalo likakhala malo amodzi, wosafalikira,
chimenecho ndi chipsera cha chithupsacho, ndipo wansembe alengeze
kuti munthuyo ndi woyera.

24 "Munthu akakhala ndi bala lamoto pa khungu lake, ndipo
chilonda cha balalo chikasanduka banga loyera mofiirira kapena loyera,
25 wansembe aonetsetse bangalo, ndipo ngati ubweya wa pa bangapo
usanduka woyera, ndipo balalo lioneka kuti ndi lozama, limenelo ndi
khate lomwe latuluka pa balalo. Wansembe alengeze kuti munthuyo ndi
wodetsedwa. Limenelo ndi khate la pa khungu. 26 Koma ngati wansembe
waonetsetsa balalo ndipo palibe ubweya woyera, ndipo ngati balalo
silinazame ndi kuti lazirala, wansembe amuyike padera wodwalayo kwa
masiku asanu ndi awiri. 27 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri wansembe amuo-
nenso wodwalayo, ndipo ngati bangalo lafalikira pa khungu, wansembe
alengeze kuti munthuyo ndi wodetsedwa. Limenelo ndi khate. 28 Koma
ngati bangalo likhala pa malo amodzi wosafalikira pa khungu, ndipo
lazimirira, limenelo ndi thuza la bala lamoto, ndipo wansembe alengeze
kuti munthuyo ndi woyera. Chimenecho ndi chipsera chamoto.

29 "Mwamuna kapena mkazi akakhala ndi nthenda kumutu kapena ku
chibwano, 30 wansembe aonetsetse balalo ndipo likaoneka kuti lazama,
ndipo ubweya wa pamalopo wasanduka wachikasu ndi wonyololoka,
wansembe alengeze kuti munthuyo ndi wodetsedwa. Zimenezo ndi
mfundu zonyerenyetsa, khate lakumutu kapena ku chibwano. 31 Koma
wansembe akaonetsetsa mfundu zonyerenyetsazo, ndipo zikaoneka kuti
sizinazame ndi kuti palibe ubweya wakuda, wansembe amuyike padera
munthuyo kwa masiku asanu ndi awiri. 32 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri
wansembe aonetsetsenso mfundu zonyerenyetsazo, ndipo ngati sizinafa-
likire ndipo palibe ubweya wachikasu pamalopo ndiponso sizinazame,
33 wodwalayo ametedwe, koma pamene pali mfunduyo pasametedwe.
Wansembe amuyike padera munthuyo kwa masiku enanso asanu ndi
awiri. 34 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri wansembe aonetsetsenso mfundu
zonyerenyetsazo ndipo ngati sizinafalikire pa khungu ndi kuti sizinazame,

wansembe alengeze kuti munthuyo ndi woyera. Tsono achape zovala
zake, ndipo adzakhala woyera. 35 Koma mfundu zonyerenyetsazo zikafa-
likira pa khungu, wansembe atalengeza kuti ndi woyera, 36 wansembe
amuonetsetsenso wodwalayo ndipo ngati mfunduzo zafalikira pa khungu,
iye asalabadirenso zoyang'ana ngati ubweya uli wachikasu. Munthuyo
ndi wodetsedwa. 37 Koma ngati wansembe waonetsetsa kuti mfunduzo
sizinasinthe ndipo ubweya wakuda wamera pa mfundupo, ndiye kuti
wodwalayo wachira. Tsono wansembe alengeze kuti munthuyo ndi
woyeretsedwa.

38 "Mwamuna kapena mkazi akakhala ndi mawanga woyera pa khungu,
39 wansembe aonetsetse mawangawo, ndipo ngati ali otuwa, ndiye kuti ndi
mibuko chabe yotuluka pa khungu. Munthuyo ndi woyera.

40 "Tsitsi la munthu likayoyoka kumutu ndiye kuti ndi dazi limenelo
koma munthuyo ndi woyeretsedwa. 41 Ngati tsitsi lake layoyoka chapam-
phumi ndiye kuti ndi dazi la pa chipumi limenelo koma munthuyo ndi
woyera. 42 Koma ngati pa dazi la pamutu kapena la pa chipumi pakhala
chithupsa choyera mofiirira, ndiye kuti ndi khate limenelo lochokera
mu dazi la pamutu lija kapena pa chipumi lija. 43 Tsono wansembe
amuonetsetse wodwalayo ndipo ngati chithupsa cha pa dazi lapankhongo
kapena pa dazi lapachipumicho ndi choyera mofiirira monga nthenda
ya khate imaonekera, 44 ndiye kuti munthuyo ali ndi khate, motero
ndi wodetsedwa. Wansembe alengeze kuti munthuyo ndi wodetsedwa
chifukwa cha chithupsa cha pamutu pakepo.

45 "Munthu wa khate lotere avale sanza, tsitsi lake alilekerere, aphimbe
mlomo wake wapamwamba ndipo azifuwula kuti, 'Ndine wodetsedwa,
ndine wodetsedwa!' 46 Munthu wodwalayo adzakhala wodetsedwa kwa
nthawi yonse imene ali ndi nthendayo. Iye ayenera kumakhala payekha
kunja kwa msasa.

### *Malamulo a Nguwi ya pa Zovala*

47 "Nsalu iliyonse ikakhala ndi nguwi, 48 kaya ndi chovala chopangidwa
ndi nsalu yathonje kapena yaubweya, yoluka ndi thonje kapena ubweya,
yachikopa kapena yopangidwa ndi chikopa, 49 ndipo ngati pamalo pamene
pachita nguwiyo pali ndi maonekedwe obiriwira kapena ofiirira imeneyo
ndi nguwi yoyipitsa chovala ndipo chovalacho chikaonetsedwe kwa
wansembe. 50 Wansembeyo ayionetsetse nguwiyo ndipo chovalacho
achiyike padera kwa masiku asanu ndi awiri. 51 Pa tsiku lachisanu
ndi chiwiri ayionetsetsenso nguwiyo ndipo ngati nguwiyo yafalikira pa
chovalacho, chathonje kapena chaubweya, kapena pa chikopacho, kaya
ndi cha ntchito ya mtundu wanji, imeneyo ndi nguwi yoopsa ndipo
chovalacho ndi chodetsedwa. 52 Wansembe atenthe chovala chathonje
kapena chaubweya chija, ngakhalenso chinthu chachikopa chija popeza
nguwiyo yachidetsa. Nguwiyo ndi yoopsa choncho chinthucho achitenthe.

53 "Koma ngati wansembe akayang'anitsitsa nguwiyo apeza kuti sinafa-
likire pa chovalacho kapena pa chinthu chilichonse chachikopa, 54 iye
alamulire kuti chinthu choyipitsidwacho achichape. Akatero achiyike
padera kwa masiku enanso asanu ndi awiri. 55 Chovalacho chitachapidwa,
wansembe achionenso ndipo ngati nguwiyo sinasinthe maonekedwe
ake, ngakhale kuti sinafalikire, chovalacho ndi chodetsedwa ndithu.
Muchitenthe, ngakhale kuti nguwiyo ili kumbuyo kapena kumaso kwa
chinthucho. 56 Koma ngati wansembe aonetsetsa n'kupeza kuti nguwi

ija yathimbirira pa chovala chija kapena pa chinthu chachikopa chija
atachichapa, ndiye ang'ambeko chinthucho pa banga la nguwiyo. 57 Koma
ngati nguwiyo iwonekanso pa chovala chathonje kapena chaubweya ndiye
kuti nguwiyo ikufalikira. Chilichonse chimene chili ndi nguwi chiyenera
kutenthedwa. 58 Chovala chathonje kapena chaubweya, ngakhale chinthu
china chilichonse chopangidwa ndi chikopa, mukachichapa nguwi yake
n'kuchoka muchichapenso kawiri ndipo chidzakhala choyeretsedwa."

59 Amenewa ndiwo malamulo a nguwi yokhala pa chovala chaub-
weya kapena pa chovala chathonje, kapenanso pa chinthu chilichonse
chopangidwa ndi chikopa kuti muzitha kulekanitsa choyeretsedwa ndi
chodetsedwa.

# 14

*Kuyeretsedwa ku Nthenda ya Khate*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Malamulo a munthu wakhate pa tsiku la
kuyeretsedwa kwake ndi awa: Abwere naye kwa wansembe. 3 Wansembe
atuluke kunja kwa msasa ndipo amuonetsetse wodwalayo. Ngati munthu
wakhateyo wachira, 4 wansembe alamule anthu kuti amutengere wodwala
woti ayeretsedweyo, mbalame zamoyo ziwiri zomwe Ayuda amaloledwa
kudya, nthambi yamkungudza, kansalu kofiirira ndi kanthambi ka hisope.
5 Wansembe alamule anthuwo kuti mbalame imodzi ayiphere mu m'phika
wa dothi pamwamba pa madzi abwino. 6 Kenaka wansembe atenge
mbalame yamoyo ija ndi kuyinyika pamodzi ndi nthambi yamkungudza,
kansalu kofiirira ndi kanthambi ka hisope kaja m'magazi ambalame imene
anayiphera pamwamba pa madzi abwino. 7 Wansembe awaze magazi
kasanu ndi kawiri pa munthu woti amuyeretse khateyo ndipo alengeze
kuti munthuyo ndi woyeretsedwa. Kenaka wansembe awulutsire ku
thengo mbalame yamoyoyo.

8 "Munthu amene wayeretsedwa uja achape zovala zake, amete tsitsi
lake lonse, ndipo asambe m'madzi. Akatero adzakhala woyeretsedwa.
Atatha zimenezi munthuyo apite ku msasa wake koma akhale kunja kwa
msasawo kwa masiku asanu ndi awiri. 9 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri
amete tsitsi lake lonse: amete kumutu, ndevu zake, nsidze zake pamodzi
ndi tsitsi lina lonse. Kenaka achape zovala zake ndi kusamba m'madzi,
ndipo adzakhala woyeretsedwa.

10 "Pa tsiku lachisanu ndi chitatu munthuyo atenge ana ankhosa aamuna
awiri ndi mwana wankhosa wamkazi wa chaka chimodzi. Zonsezi zikhale
zopanda chilema. Atengenso chopereka chachakudya cha ufa wosalala
wa makilogalamu atatu wosakaniza ndi mafuta wokwana limodzi mwa
magawo atatu a lita. 11 Wansembe amene ati ayeretse munthu wodwalayo
amuyimitse munthuyo ali ndi zopereka zake zonse pamaso pa Yehova pa
khomo la tenti ya msonkhano.

12 "Ndipo wansembe atenge mwana wankhosa wamwamuna mmodzi
ndi kumupereka kuti akhale nsembe yopepesera kupalamula, pamodzi ndi
mafuta wokwana limodzi mwa magawo atatu a lita. Wansembe aziweyule
zonsezi pamaso pa Yehova kuti zikhale chopereka choweyula. 13 Mwana
wankhosayo amuphere pa malo amene amaphera nsembe yopepesera
machimo ndi nsembe yopsereza, kutanthauza malo opatulika. Monga zi-
makhalira ndi chopereka chopepesera machimo, chopereka ichi ndi chake
cha wansembe ndipo ndi chopereka choyera kopambana. 14 Wansembe
atengeko magazi a nsembe yopepesera kupalamula ndi kuwapaka pa

msonga pa khutu lakumanja la munthu woti ayeretsedweyo. Apakenso
pa chala chachikulu cha ku dzanja lamanja, ndi chala chachikulu cha ku
phazi lakumanja. [15] Wansembe atengeko mafuta pang'ono, n'kuwathira
m'dzanja lake lamanzere, [16] aviyike chala chake cha ku dzanja lamanja
m'mafuta amene ali m'dzanja lamanzerewo, ndi kuwaza mafutawo ndi
chala chakecho kasanu ndi kawiri pamaso pa Yehova. [17] Wansembe
apake mafuta otsala m'dzanja lake pa khutu lakumanja la munthu amene
akuyeretsedwayo. Awapakenso pa chala chake chachikulu cha ku dzanja
lamanja ndiponso pa chala chake chachikulu cha ku phazi lakumanja,
pamalo pamene anali atapakapo magazi a nsembe yopepesera kupalamula
paja. [18] Mafuta onse otsala m'dzanja la wansembe awathire pamutu
pa munthu woti ayeretsedwe uja, ndipo potero adzachita mwambo
womupepesera pamaso pa Yehova.

[19] "Kenaka wansembe apereke nsembe yopepesera machimo kuti achite
mwambo womupepesera munthu woti ayeretsedwe khate lake uja. Atatha
kuchita zimenezi, wansembe aphe nyama ya nsembe yopsereza [20] ndi
kuyipereka pa guwa, pamodzi ndi nsembe yachakudya. Akatero ndiye kuti
wansembe wachita mwambo wopepesera munthu wodzayeretsedwayo,
ndipo adzakhala woyera.

[21] "Ngati munthu woti ayeretsedweyo ndi wosauka ndipo sangathe
kupeza zinthu zimenezi, apereke mwana wankhosa wamwamuna monga
nsembe yopepesera kupalamula ndipo ayiweyule pochita mwambo wom-
upepesera. Aperekenso kilogalamu imodzi ya ufa wosalala osakaniza ndi
mafuta kuti ikhale nsembe yachakudya, pamodzi ndi mafuta wokwanira
limodzi mwa magawo atatu a lita. [22] Aperekenso njiwa ziwiri kapena
mawunda awiri zomwe iye angathe kuzipeza. Imodzi ikhale nsembe
yopepesera machimo, ndi inayo ikhale ya nsembe yopsereza.

[23] "Pa tsiku lachisanu ndi chitatu zonsezo abwere nazo kwa wansembe,
pa khomo pa tenti ya msonkhano, pamaso pa Yehova kuti munthuyo
ayeretsedwe. [24] Wansembe atenge mwana wankhosa wopereka nsembe
yopepesera kupalamula, pamodzi ndi mafuta aja, ndipo aziweyule kuti
zikhale nsembe yoweyula pamaso pa Yehova. [25] Wansembe aphe
nkhosa yopereka nsembe yopepesera kupalamula ndipo atenge magazi
ake ndi kuwapaka pa msonga ya khutu lakumanja la munthu amene
ayeretsedweyo. Awapakenso pa chala chachikulu cha ku dzanja lamanja,
ndiponso pa chala chachikulu cha ku phazi lakumanja. [26] Kenaka
wansembe athire mafuta m'dzanja lake lamanzere, [27] ndipo ndi chala
chake cha ku dzanja lamanja awaze mafutawo kasanu ndi kawiri pamaso
pa Yehova. [28] Apakenso mafuta omwewo amene ali m'dzanja lake
lamanja pa msonga ya khutu la kudzanja lamanja la munthu amene
akuyeretsedwayo. Apakenso pa chala chachikulu cha phazi lakumanja,
pamalo pamene anapakapo magazi a nsembe yopepesera kupalamula.
[29] Mafuta onse otsala amene ali m'dzanja la wansembe awapake pamutu
pa munthu amene ayeretsedweyo kuti amuchitire mwambo wopepesera
machimo pamaso pa Yehova. [30] Ndipo munthuyo apereke njiwa ziwiri
kapena mawunda ankhunda awiri, molingana ndi mmene anapezeramo,
[31] imodzi ikhale ya nsembe yopepesera machimo ndipo inayo ikhale ya
nsembe yopsereza, pamodzi ndi chopereka chachakudya. Akatero ndiye
kuti wansembe wachita mwambo wopepesera machimo a munthu woti
ayeretsedwe.

32 “Amenewa ndi malamulo a munthu wakhate amene alibe zinthu zoti
apereke pamene akuyeretsedwa.

### *Za Ndere za M’nyumba*

33 “Yehova anawuza Mose ndi Aaroni kuti, 34 Mukakalowa m’dziko
la Kanaani limene ndikukupatsani kuti likhale lanu, ndipo Ine ndikak-
abweretsa ndere zoyanga m’nyumba m’dziko limenelo, 35 mwini wake
nyumbayo adzapite kwa wansembe ndi kukamuwuza kuti, ‘Ndaona
chinthu chooneka ngati ndere m’nyumba mwanga.’ 36 Tsono wansembe
alamule kuti anthu atulutse zinthu zonse m’nyumbamo iye asanalowemo
ndi kukaonetsetsa ndereyo kuti m’nyumbamo musapezeke chinthu choti
achitchule chodetsedwa. Izi zitachitika, wansembe alowe m’nyumbamo
ndi kukaonamo. 37 Iye aonetsetse nderezo. Tsono akapeza kuti
nderezo zili m’khoma la nyumba, ndipo ngati zili ndi mawanga obiriwira
kapena ofiirira, komanso zikuoneka kuti zalowerera mpaka m’kati mwa
khoma, 38 wansembe atuluke m’nyumbamo ndi kupita pa khomo, ndipo
ayitseke nyumbayo masiku asanu ndi awiri. 39 Pa tsiku la chisanu
ndi chiwiri wansembe abwerenso kudzayang’ana m’nyumbamo. Ngati
ndere yafalikira m’makoma a nyumbayo, 40 wansembe alamule kuti anthu
agumule miyala imene muli nderezo ndipo akayitaye kudzala la kunja kwa
mzinda. 41 Wansembe awuze anthu kuti apale makoma onse a m’kati mwa
nyumbayo, ndipo zopalidwazo akazitaye ku malo odetsedwa a kunja kwa
mudzi. 42 Tsono anthuwo atenge miyala ina ndi kuyilowetsa m’malo mwa
miyala imene anagumula ija ndipo atenge dothi latsopano ndi kumata
nyumbayo.

43 “Ngati ndere iwonekanso m’nyumbamo atagumula kale miyala
ndiponso atayipala kale ndi kuyimatanso, 44 wansembe apite kukayionet-
setsenso ndipo ngati nderezo zafalikira m’nyumbamo, ndiye kuti ndere
zimenezo ndi zoopsa. Nyumba imeneyo ndi yodetsedwa. 45 Agwetse
nyumbayo, ndipo miyala yake, matabwa pamodzi ndi dothi lake lonse,
zonse akazitaye kudzala lodetsedwa, kunja kwa mzinda.

46 “Aliyense amene alowa m’nyumbamo itatsekedwa adzakhala
wodetsedwa mpaka madzulo. 47 Munthu amene wagona m’nyumbamo
kapena kudyeramo ayenera kuchapa zovala zake.

48 “Koma ngati pambuyo pa kuyimata, wansembe abwera kudza-
onetsetsa m’nyumbamo napeza kuti ndereyo sinafalikire, iye alengeze
kuti nyumbayo ndi yoyeretsedwa, chifukwa ndereyo yatha. 49 Kuti
nyumbayo iyeretsedwe, mwini wake atenge mbalame ziwiri, kanthambi
kamkungudza, kansalu kofiirira ndi kachitsamba ka hisope. 50 Wansembe
aphe mbalame imodzi pamwamba pa madzi abwino mu m’phika wa
dothi. 51 Kenaka atenge kanthambi kamkungudza, kachitsamba ka hisope,
kansalu kofiirira pamodzi ndi mbalame yamoyo ija, zonsezi aziviyike
m’magazi a mbalame yophedwa ija, ndiponso m’madzi abwino aja, ndipo
awaze nyumbayo kasanu ndi kawiri 52 Akatero ndiye kuti wayeretsa
nyumbayo ndi magazi a mbalame, madzi abwino, mbalame yamoyo,
kanthambi kamkungudza, kachitsamba ka hisope ndi kansalu kofiirira.
53 Kenaka ayiwulutsire mbalame yamoyo ija kuthengo, kunja kwa mzinda.
Pamenepo ndiye kuti wansembe wachita mwambo wopepesera nyum-
bayo, ndipo idzakhala yoyeretsedwa.”

54 Amenewa ndiwo malamulo a nthenda ya khate, bala lonyerenyetsa,
55 nguwi za pa zovala, ndere za m’nyumba, 56 khate la chithupsa, khate

la m'buko ndi khate la banga 57 kuti mudziwe ngati chinthucho ndi
choyeretsedwa kapena chodetsedwa.

Amenewa ndiwo malamulo a nthenda zonse za khate.

# 15

*Zonyansa Zotuluka M'thupi*

1 Yehova anawuza Mose ndi Aaroni kuti, 2 "Yankhulani ndi Aisraeli ndipo
muwawuze kuti, 'Mwamuna aliyense akakhala ndi nthenda yotulutsa
mafinya ku maliseche ake, zotulukazo ndi zonyansa ndithu. 3 Lamulo
lokhudza kudziyipitsira ndi zotuluka ku maliseche a munthu nali:
Malisechewo akamatulukabe mafinya, kaya aleka, munthuyo adzakhala
wodetsedwa:

4 " 'Bedi lililonse limene munthu wotulutsa mafinyayo agonapo,
ndiponso chinthu chilichonse chimene akhalepo chidzakhala
chodetsedwa. 5 Aliyense wokhudza bedi la munthuyo achape zovala zake
ndi kusamba. Komabe adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo. 6 Aliyense
wokhala pa chinthu chimene munthu wotulutsa mafinyayo anakhalapo,
achape zovala zake ndi kusamba. Komabe adzakhala wodetsedwa mpaka
madzulo.

7 " 'Aliyense wokhudza thupi la munthu amene akutulutsa mafinyayo
achape zovala zake ndi kusamba. Komabe adzakhala wodetsedwa mpaka
madzulo.

8 " 'Munthu wotulutsa mafinya akalavulira malovu munthu wina amene
ndi woyeretsedwa, munthu ameneyo achape zovala zake ndi kusamba.
Komabe adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo.

9 " 'Chilichonse chimene munthuyo akhalira akakwera pa kavalo chidza-
khala chodetsedwa. 10 Ndipo aliyense wokhudza chimene anakhalira
munthuyo adzakhala wodetsedwanso mpaka madzulo. Aliyense wonya-
mula chinthucho achape zovala zake ndi kusamba. Komabe adzakhala
wodetsedwa mpaka madzulo.

11 " 'Munthu wotulutsa mafinyayo akakhudza munthu aliyense
asanasambe m'manja, wokhudzidwayo achape zovala zake ndi kusamba.
Komabe adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo.

12 " 'M'phika wadothi umene munthu wotulutsa mafinyayo wakhudza
awuphwanye, ndipo chiwiya chilichonse chamtengo achitsuke ndi madzi.

13 " 'Munthu wotulutsa mafinyayo akaona kuti wachira, awerenge
masiku asanu ndi awiri akuyeretsedwa kwake kenaka achape zovala
zake ndi kusamba pa kasupe, ndipo adzayeretsedwa. 14 Pa tsiku la
chisanu ndi chitatu atenge njiwa ziwiri kapena mawunda a nkhunda
awiri ndi kubwera nazo pamaso pa Yehova pa khomo pa tenti ya
msonkhano ndipo azipereke kwa wansembe. 15 Wansembe apereke
zimenezo: imodzi ikhale nsembe yopepesera machimo ndipo inayo
ikhale ya nsembe yopsereza. Pamenepo ndiye kuti wansembeyo wachita
mwambo wopepesera machimo a munthu wotulutsa mafinya uja pamaso
pa Yehova.

16 " 'Mwamuna akataya pansi mbewu yake yaumuna, asambe thupi
lake lonse. Komabe adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo. 17 Chovala
chilichonse kapena chikopa chilichonse pomwe pagwera mbewu yau-
munayo achichape, komabe chidzakhala chodetsedwa mpaka madzulo.
18 Mwamuna akagona ndi mkazi wake nataya mbewu yake yaumuna, onse
awiriwo asambe. Komabe adzakhala odetsedwa mpaka madzulo.

19 “ ‘Mkazi akakhala wosamba ndipo ikakhala kuti ndi nthawi yake
yeniyeni yosamba, adzakhala wodetsedwa masiku asanu ndi awiri.
Aliyense amene adzamukhudza adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo.

20 “ ‘Chilichonse chimene mkaziyo agonera pa nthawi yake yosamba
chidzakhala chodetsedwa, ndipo chilichonse chimene adzakhalira chidza-
khalanso chodetsedwa. 21 Aliyense wokhudza bedi lake achape zovala
zake ndi kusamba, komabe adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo.
22 Aliyense wokhudza chimene wakhalapo achape zovala zake ndi
kusamba, komabe adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo. 23 Kaya
ndi bedi kapena chinthu china chilichonse chimene anakhalapo, ngati
munthu wina akhudza chinthucho, munthuyo adzakhala wodetsedwa
mpaka madzulo.

24 “ ‘Mwamuna aliyense akagona naye ndipo magazi osamba kwake ndi
kumukhudza, munthuyo adzakhala wodetsedwa masiku asanu ndi awiri,
ndipo bedi limene wagonapo lidzakhalanso lodetsedwa.

25 “ ‘Mkazi akataya magazi masiku ambiri, wosakhala pa nthawi
yake yosamba, kapena akamasambabe kupitirira nthawi yake yosamba,
mkaziyo adzakhala wodetsedwa nthawi yonse imene akutaya magazi,
monga momwe amakhalira pa masiku ake osamba. 26 Bedi lililonse limene
mkaziyo adzagonapo pa masiku onse pamene ali wotaya magazi, ndiponso
chilichonse chimene wakhalira chidzakhala chodetsedwa monga mmene
chimakhalira chodetsedwa pa nthawi yake yosamba. 27 Aliyense amene
adzakhudza zinthu zimenezo adzakhala wodetsedwa ndipo ayenera
kuchapa zovala zake ndi kusamba, komabe adzakhala wodetsedwa mpaka
madzulo.

28 “ ‘Nthawi yosamba ikatha, mkaziyo awerenge masiku asanu ndi
awiri, ndipo masikuwo akatha adzakhala woyeretsedwa. 29 Pa tsiku
lachisanu ndi chitatu, mkaziyo atenge njiwa ziwiri kapena mawunda
awiri, ndipo abwere nazo kwa wansembe pa khomo la Tenti ya
Msonkhano. 30 Wansembe apereke imodzi kuti ikhale nsembe yopepesera
machimo ndipo inayo ikhale ya nsembe yopsereza. Pamenepo ndiye kuti
wansembeyo wachita mwambo wopepesera mkaziyo pamaso pa Yehova
chifukwa cha matenda ake wosamba aja.

31 “ ‘Choncho muwayeretsa ana a Israeli n’kudetsedwa kwawo kuti
angafe pochita tchimo lowadetsa limene polichita limadetsa malo anga
wokhalamo amene ali pakati pawo.’ ”

32 Amenewa ndi malamulo a munthu amene akutuluka mafinya ku-
maliseche kwake, komanso a munthu aliyense amene wadetsedwa ndi
mbewu yaumuna, 33 mkazi wodwala chifukwa cha msambo komanso a
mwamuna kapena mkazi amene akutulutsa mafinya kumaliseche kwake
ndi mwamuna wogona ndi mkazi amene akusamba.

# 16

*Tsiku la Mwambo Wopepesera Machimo*

1 Atafa ana awiri a Aaroni amene anaphedwa atapita pamaso pa
Yehova mosayenera, Yehova anayankhula ndi Mose. 2 Yehova anawuza
Mose kuti, “Uza mchimwene wako Aaroni kuti asamalowe ku Malo
Wopatulika, kuseri kwa katani, pamaso pa chivundikiro cha Bokosi la
Chipangano nthawi iliyonse imene akufuna kuopa kuti angadzafe, pakuti
Ine ndimaoneka mu mtambo umene uli pamwamba pa chivundikiro cha
Bokosi la Chipangano.

3 “Aaroni azilowa Malo Wopatulika Kwambiri motere: azitenga mwana
wang’ombe wamwamuna kuti akhale nsembe yopepesera machimo ndi
nkhosa yayimuna kuti ikhale nsembe yopsereza. 4 Azivala mwinjiro
wopatulika wa nsalu yosalala, azivalanso kabudula wa m’kati wa nsalu
yosalala, azimanga lamba wa nsalu yosalala, ndipo avalenso nduwira ya
nsalu yosalala kumutu. Zimenezi ndi nsalu zopatulika ndipo atasamba
thupi lonse azivala zimenezi. 5 Kuchokera pa gulu la Aisraeli, Aaroni
azitenga mbuzi zazimuna ziwiri kuti zikhale nsembe yopepesera machimo
ndi nkhosa yayimuna kuti ikhale nsembe yopsereza.

6 “Aaroni apereke ng’ombe yayimuna kuti ikhale yopepesera machimo
a iye mwini kuti achite mwambo wopepesera machimo ake pamodzi ndi
a banja lake. 7 Kenaka atenge mbuzi ziwiri zija ndipo aziyimike pamaso
pa Yehova pa khomo la tenti ya msonkhano. 8 Aaroni ndiye achite maere
pa mbuzi ziwirizo kuti imodzi ikhale ya Yehova, ndipo inayo ikhale ya
Azazele. 9 Aaroni abwere ndi mbuzi imene maere aonetsa kuti ndi ya
Yehova, ndipo apereke kuti ikhale nsembe yopereka chifukwa cha tchimo.
10 Koma mbuzi imene maere aonetsa kuti ndi yosenza machimo, apereke
ya moyo pamaso pa Yehova, kuti achite mwambo wopepesera machimo
pa mbuziyo poyitumiza ku chipululu kuti ikhale ya Azazele.

11 “Aaroni apereke ng’ombe yayimuna kuti ikhale nsembe yopepesera
machimo ake. Ndiye achite mwambo wopepesera machimo a iye mwini
wake pamodzi ndi banja lake. Pambuyo pake aphe ng’ombe yopepesera
machimo ake aja. 12 Kenaka iye atenge chofukizira chodzaza ndi makala
a moto ochokera pa guwa lansembe pamaso pa Yehova. Atengenso lubani
wonunkhira ndi woperapera wokwanira manja awiri, ndipo alowe naye
kuseri kwa katani. 13 Athire lubani pa moto pamaso pa Yehova kuti
utsi wa lubaniyo uphimbe chivundikiro chimene chili pamwamba pa
Bokosi la Chipangano, kuti Aaroniyo asafe. 14 Ndipo atenge magazi ena
a ng’ombeyo, awawaze ndi chala chake pa chivundikiro cha kummawa;
kenaka awaze magaziwo ndi chala chake kasanu ndi kawiri patsogolo pa
chivundikirocho.

15 “Kenaka Aaroni aphe mbuzi ya nsembe yopepesera machimo a
anthu, ndipo magazi ake alowe nawo kuseri kwa katani ndi kuchita
chimodzimodzi monga anachitira ndi magazi a ng’ombe aja: Aaroni
awaze magaziwo pa chivundikiro chija ndi patsogolo pa chivundikirocho.
16 Pamenepo ndiye kuti wansembeyo wachita mwambo wopepesera ku
Malo Wopatulika chifukwa cha kudetsedwa ndi kuwukira kwa Aisraeli pa
machimo ena aliwonse amene achita. Achite chimodzimodzi ndi tenti ya
msonkhano imenenso ili yodetsedwa chifukwa cha machimo awo. 17 Mu
tenti ya msonkhano musakhale munthu ndi mmodzi yemwe nthawi imene
Aaroni akupita kukachita mwambo wopepesera ku Malo Wopatulika
mpaka atatulukako. Musakhale munthu mu tenti ya msonkhano mpaka
atachita mwambo wopepesera machimo a iye mwini wake, banja lake ndi
gulu lonse la Aisraeli.

18 “Kenaka, Aaroniyo akatuluka apite ku guwa limene lili pamaso
pa Yehova ndi kulichitira mwambo wolipepesera. Atengeko magazi a
ng’ombe yayimuna ndiponso magazi a mbuzi ndi kuwapaka pa nyanga
zonse za guwa lansembe. 19 Magazi ena awawaze pa guwalo ndi chala
chake kasanu ndi kawiri kuliyeretsa ndi kulipatula kuchotsa zodetsa za
Aisraeli.

20 “Aaroni akatsiriza mwambo wopepesera Malo Wopatulika, tenti
ya msonkhano ndi guwa, azibwera ndi mbuzi yamoyo kudzayipereka

nsembe. 21 Aaroni asanjike manja ake pa mutu wa mbuziyo ndipo awulule
pa mbuziyo zoyipa zonse ndi zowukira zonse za Aisraeli, kutanthauza
machimo awo onse. Machimowo awayike pa mutu wa mbuziyo. Kenaka
munthu amene anasankhidwa athamangitsire mbuziyo ku chipululu.
22 Mbuziyo isenze machimo awo onse ndi kupita nawo kutali ndipo
munthuyo aleke mbuziyo kuti ipite ku chipululuko.

23 "Pambuyo pake Aaroni alowe mu tenti ya msonkhano ndi kuvula
zovala zosalala zija zimene anavala polowa ku Malo Wopatulika ndi
kuzisiya komweko. 24 Asambe thupi lonse ku Malo Wopatulika ndi kuvala
zovala zake za nthawi zonse. Kenaka atuluke ndi kukapereka nsembe
yopsereza ya iye mwini, ndiponso nsembe yopsereza yoperekera anthu.
Akatero ndiye kuti wachita mwambo wopepesera machimo a iye mwini
wake ndi a anthu. 25 Mafuta a nyama yopepesera machimo awatenthe pa
guwa lansembe.

26 "Tsono munthu amene anaperekeza mbuzi yosenza machimo ija
achape zovala zake ndi kusamba. Pambuyo pake alowe ku msasa.
27 Ng'ombe ndi mbuzi zoperekera nsembe yopepesera machimo zimene
magazi ake anabwera nawo kuti achitire mwambo wopepesera Malo
Wopatulika, azitulutsire kunja kwa msasa. Koma zikopa zake, nyama yake
ndi matumbo ake azitenthe. 28 Munthu amene azitenthe achape zovala
zake ndi kusamba. Pambuyo pake alowe mu msasa.

29 "Ili likhale lamulo lanu lamuyaya: Mwezi wachisanu ndi chiwiri, pa
tsiku la khumi la mwezi, mugonje pamaso pa Yehova. Musamagwire
ntchito iliyonse, kaya ndinu mbadwa kapena mlendo amene akukhala
pakati panu, 30 chifukwa tsiku limeneli kudzachitika mwambo wopepesera
machimo anu, kukuyeretsani kuti mukhale oyeretsedwa ku machimo anu
pamaso pa Yehova. 31 Limeneli ndi tsiku lanu la Sabata lopumula, ndipo
muzigonja pamaso pa Yehova. Limeneli ndi lamulo lanu la muyaya.
32 Wansembe amene wadzozedwa ndi kupatulidwa kuti akhale wansembe
kulowa m'malo mwa abambo ake ndiye azichita mwambo wopepesera
machimo atavala zovala zake zosalala ndi zopatulika. 33 Adzachite
mwambo wopepesera machimo Malo Wopatulika, tenti ya msonkhano
ndi guwa lansembe. Adzachitenso mwambo wopepesera anzake ndi gulu
lonse la anthu.

34 "Ili likhale lamulo lanu lamuyaya. Mwambo wopepesera machimo
uzichitika kamodzi pa chaka chifukwa cha machimo a anthu onse."
Ndipo Mose anachita monga momwe Yehova analamulira.

# 17

*Za Kusadya Magazi*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Uza Aaroni ndi ana ake, pamodzi
ndi Aisraeli onse kuti, 'Chimene Yehova walamula ndi ichi: 3 Mwisraeli
aliyense amene apha ng'ombe, mwana wankhosa kapena mbuzi mu
msasa kapena kunja kwa msasa, 4 m'malo mobwera nayo pa khomo la
tenti ya msonkhano pamaso pa Yehova ndi kuyipereka kuti ikhale nsembe
ya Yehova, ameneyo wapalamula mlandu wa magazi, wakhetsa magazi
ndipo ayenera kuchotsedwa pakati pa anthu anzake. 5 Izi zili choncho
kuti Aisraeli azibwera ndi nyama zawo za nsembe zimene akanaphera
ku malo kwina kulikonse. Aisraeli azibwera nazo nyamazo kwa Yehova,
kwa wansembe wokhala pa khomo la tenti ya msonkhano ndipo aziphere
pomwepo kuti zikhale nsembe za chiyanjano. 6 Wansembe awaze magazi

ake pa guwa la Yehova limene lili pa khomo la tenti ya msonkhano
ndipo atenthe mafuta ake kuti atulutse fungo lokomera Yehova. [7] Motero
asadzapherenso nsembe fano la mbuzi limene amachita nalo zadama.
Limeneli ndi lamulo la muyaya kwa iwo ndi mibado ya m'tsogolo.' "

[8] "Uwawuze kuti, 'Mwisraeli aliyense kapena mlendo amene amakhala
pakati pawo akapereka nsembe yopsereza kapena nsembe ina iliyonse
[9] popanda kubwera nayo pa khomo la tenti ya msonkhano kudzayipereka
pamaso pa Yehova, munthu ameneyo achotsedwe pakati pa anthu
anzake.' "

[10] "Mwisraeli aliyense kapena mlendo aliyense wokhala pakati panu
amene adya magazi, ndidzamufulatira ndipo ndidzamuchotsa pakati pa
anthu anzake. [11] Pakuti moyo wa cholengedwa chilichonse uli m'magazi,
ndipo ndawupereka kwa inu kuti muzichitira mwambo wopepesera
machimo a moyo wanu pa guwa. Pajatu magazi ndiwo amachotsa
machimo chifukwa moyo uli m'menemo. [12] Choncho ndikuwawuza
Aisraeli kuti, 'Pasapezeke aliyense wa inu wodya magazi, ngakhale mlendo
wokhala pakati panu.' "

[13] "Mwisraeli aliyense kapena mlendo aliyense wokhala pakati panu
amene amasaka ndi kupha nyama zakuthengo kapena mbalame zimene
amadya, ataye magazi ake pansi ndi kuwakwirira ndi dothi, [14] chifukwa
moyo wa cholengedwa chilichonse uli m'magazi ake. N'chifukwa
chake ndinawawuza Aisraeli kuti, 'Musamadye magazi a cholengedwa
chilichonse, chifukwa moyo wa cholengedwa chilichonse uli m'magazi.
Aliyense wodya magaziwo ayenera kuchotsedwa pakati pa anthu anzake.

[15] " 'Munthu aliyense, kaya ndi mbadwa kapena mlendo, amene amadya
chilichonse chofa chokha, kapena chojiwa ndi zirombo, achape zovala
zake ndi kusamba, komabe adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo.
Kenaka adzakhala woyeretsedwa. [16] Koma ngati sachapa zovala zake ndi
kusamba, adzasenzabe machimo ake.' "

# 18

*Kugonana Koletsedwa*

[1] Yehova anawuza Mose kuti, [2] "Yankhula ndi Aisraeli ndipo uwawuze
kuti, 'Ine ndine Yehova Mulungu wanu. [3] Musamachite zomwe ama-
chita anthu a ku Igupto kumene munkakhala kuja, ndiponso musama-
chite zomwe amachita anthu a ku Kanaani kumene ndikukupititsani.
Musatsatire miyambo yawo. [4] Inu muzimvera malamulo anga ndipo
muzisamalitsa kutsatira malangizo anga. Ine ndine Yehova Mulungu
wanu. [5] Choncho sungani malangizo ndi malamulo anga, popeza munthu
amene amvera zimenezi adzakhala ndi moyo. Ine ndine Yehova.

[6] " 'Munthu aliyense asagonane ndi wachibale wake. Ine ndine Yehova.

[7] " 'Usachititse manyazi abambo ako pogonana ndi amayi ako. Iwo ndi
amayi ako. Usagonane nawo.

[8] " 'Usagonane ndi mkazi wa abambo ako (osakhala amayi okubala).
Ukatero ukuchititsa manyazi abambo ako.

[9] " 'Usagonane ndi mlongo wako, mwana wamkazi wa abambo ako,
kapena mwana wamkazi wa amayi ako, kaya anabadwira m'nyumba
mwanu kapena kwina.

[10] " 'Usagonane ndi mdzukulu wako: mwana wa mwana wako wamwa-
muna kapena mwana wa mwana wako wamkazi. Kutero n'kudzichotsa
ulemu.

11 “ ‘Usagonane ndi mwana wamkazi wa mkazi wa abambo ako, amene
abambo akowo anabereka; popeza ameneyo ndi mlongo wako.
12 “ ‘Usagonane ndi mlongo wa abambo ako; popeza ameneyo ndi thupi
limodzi ndi abambo ako.
13 “ ‘Usagonane ndi mchemwali wa amayi ako chifukwa ameneyo ndi
thupi limodzi ndi amayi ako.
14 “ ‘Usachititse manyazi mchimwene wa abambo ako pogonana ndi
mkazi wake popeza amenewo ndi azakhali ako.
15 “ ‘Usagonane ndi mpongozi wako popeza ameneyo ndi mkazi wa
mwana wako. Choncho usamuchititse manyazi.
16 “ ‘Usagonane ndi mkazi wa mchimwene wako popeza potero ukuchi-
titsa manyazi m’bale wakoyo.
17 “ ‘Usagonane ndi mkazi ndiponso mwana wake wamkazi. Usagonane
ndi mwana wamkazi wa mwana wake wamwamuna, kapena mwana
wamkazi wa mwana wake wamkazi. Amenewo ndi thupi limodzi ndi
mkaziyo. Kutero ndikuchita chinthu choyipa kwambiri.
18 “ ‘Usakwatire mchemwali wa mkazi wako ndi kumagonana naye
mkazi wakoyo ali moyo ngati wopikisana naye.
19 “ ‘Usamuyandikire mkazi kuti ugonane naye pa nthawi yake yosamba.
20 “ ‘Usagonane ndi mkazi wa mnzako ndi kudziyipitsa naye.
21 “ ‘Usapereke mwana wako aliyense kuti akhale nsembe yamoto kwa
Moleki ndi kuyipitsa dzina la Yehova. Ine ndine Yehova.
22 “ ‘Usagonane ndi mwamuna ngati mkazi; chimenecho ndi chinthu
chonyansa.
23 “ ‘Usagonane ndi nyama ndi kudziyipitsa nayo. Mkazi asadzipereke
kwa nyama kuti agonane nayo. Chimenecho ndi chisokonezo.
24 “ ‘Musadzidetse ndi zinthu zimenezi chifukwa umo ndi mmene
mitundu ina imene ndikuyithamangitsa pamaso panu inadzidetsera.
25 Choncho dziko linayipa ndipo ndinalilanga chifukwa cha tchimo lake.
Motero dzikolo linasanza anthu ake okhalamo. 26 Koma inu mukasunge
malangizo ndi malamulo anga. Mbadwa ndiponso alendo amene akukhala
pakati panu asakachite china chilichonse cha zinthu zonyansazi, 27 pakuti
zinthu zonsezi ndi zomwe ankachita anthu amene ankakhala m’dzikomo
inu musanafike, ndipo dziko linayipitsidwa. 28 Koma inu musachite
zimenezi kuti dziko lingakusanzeni mutaliyipitsa monga linasanzira
mitundu imene imakhalamo inu musanafike.
29 “ ‘Aliyense wochita zinthu zonyansa zimenezi achotsedwe pakati
pa anthu anzake. 30 Choncho mverani malangizo anga oletsa kuchita
miyambo yonyansayi imene ankatsatira anthu amene analipo inu mu-
sanafike ndi kudziyipitsa nayo. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.’ ”

# 19

*Malamulo Osiyanasiyana*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 “Uza gulu lonse la Aisraeli kuti, ‘Khalani
oyera mtima chifukwa Ine, Yehova Mulungu wanu, ndine Woyera.
3 “ ‘Aliyense mwa inu azilemekeza abambo ake ndi amayi ake. Ndipo
muzisunga masabata anga. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.
4 “ ‘Musatembenukire ku mafano kapena kudzipangira nokha milungu
ya zitsulo zosungunula. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.
5 “ ‘Pamene mukupereka nsembe yachiyanjano kwa Yehova, muyipereke
mwanjira yoti ilandiridwe. 6 Nsembe izidyedwa tsiku lomwe

mwayiperekalo kapena mmawa mwake. Chilichonse chotsala mpaka
tsiku lachitatu chiyenera kutenthedwa. 7 Ngati mudya choperekacho
tsiku lachitatu, ndiye kuti mwachita chonyansa ndipo chakudyacho
sichidzalandiridwa. 8 Munthu aliyense amene adya chakudyacho
adzasenza machimo ake chifukwa wayipitsa chinthu chimene ndi choyera kwa Yehova. Munthu ameneyo achotsedwe pakati pa anthu anzake.

9 “ ‘Pamene mukolola zinthu m’munda mwanu musakolole mpaka
m’mphepete mwa munda, ndipo musatole khunkha lake. 10 Musakolole
mphesa zonse m’munda wanu wa mpesa kapena kutola mphesa zakugwa m’mundamo. Zimenezi muzisiyire anthu osauka ndi alendo. Ine ndine Yehova Mulungu wako.

11 “ ‘Musabe.

“ ‘Musamanamizane.

“ ‘Musachitirane zinthu mwachinyengo.

12 “ ‘Musalumbire m’dzina langa monyenga popeza kutero ndi kuyipitsa dzina la Mulungu wanu. Ine ndine Yehova.

13 “ ‘Musapsinje mnzanu kapena kumulanda zinthu zake.

“ ‘Musasunge malipiro a munthu wantchito usiku wonse mpaka mmawa.

14 “ ‘Musatemberere wosamva kapena kuyikira munthu wosaona chinthu choti apunthwe nacho patsogolo pake, koma muziopa Mulungu wanu. Ine ndine Yehova.

15 “ ‘Musamaweruze mopanda chilungamo. Musachite tsankho pakati pa osauka ndi olemera, koma muweruze mlandu wa mnzanu mwachilungamo.

16 “ ‘Musamapite uku ndi uku kunena bodza pakati pa anthu anu.

“ ‘Musachite kanthu kalikonse kamene kangadzetse imfa kwa mnzanu. Ine ndine Yehova.

17 “ ‘Musamude m’bale wanu mu mtima mwanu. Koma mudzudzuleni mnzanu moona mtima kuti musakhale wolakwa.

18 “ ‘Musamubwezere mnzanu choyipa kapena kumusungira kanthu kunkhosi, koma konda mnansi wako monga iwe mwini. Ine ndine Yehova.

19 “ ‘Muzisunga malangizo anga.

“ ‘Tsono musamalole kuti ng’ombe zanu zikwerane ndi chiweto cha mtundu wina.

“ ‘Ndiponso musamadzale mbewu za mitundu iwiri m’munda umodzi.

“ ‘Musavale chovala chopangidwa ndi nsalu za mitundu iwiri.

20 “ ‘Ngati munthu agonana ndi kapolo wamkazi amene wafunsidwa
mbeta ndi munthu wina, koma sanawomboledwe kapenanso kulandira
ufulu wake, alangidwe. Koma onsewa asaphedwe, chifukwa mkaziyo
anali asanalandire ufulu wake. 21 Koma mwamunayo abwere ndi nsembe
yopepesera kupalamula kwa Yehova pa khomo la tenti ya msonkhano.
Nsembe yake ikhale nkhosa yayimuna 22 ndipo wansembe achite nayo
mwambo wopepesera chifukwa cha kupalamula kumene anachita pamaso pa Yehova. Akatero tchimo lake lidzakhululukidwa.

23 “ ‘Mukadzalowa m’dzikomo ndi kudzala mtengo wa mtundu uliwonse
wa zipatso, zipatso zakezo mudzaziyese ngati zodetsedwa. Ndiye kuti
kwa zaka zitatu zidzakhale zoletsedwa kwa inu. Musadzazidye nthawi
imeneyi. 24 Chaka chachinayi, zipatso zake zonse zidzakhala zopatulika,
ndipo zidzakhala chopereka cha matamando kwa Yehova. 25 Koma chaka
chachisanu, mudzatha kudya zipatso zake kuti mitengoyo idzakubalireni zochuluka. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.

26 “ ‘Musadye nyama ya magazi.
“ ‘Musamawombeze kapena kuchita zamatsenga.
27 “ ‘Musamamete mduliro kapena kumeta m’mphepete mwa ndevu zanu.
28 “ ‘Musadzichekecheke pathupi panu chifukwa cha munthu wakufa kapena kudzitema mphini pa thupi lanu. Ine ndine Yehova.
29 “ ‘Musamuyipitse mwana wanu wamkazi pomusandutsa mkazi wachiwerewere. Mukatero dziko lidzasanduka la anthu achiwerewere ndi lodzaza ndi zoyipa.
30 “ ‘Muzisunga Masabata anga ndipo muzilemekeza malo anga opatulika. Ine ndine Yehova.
31 “ ‘Musamapite kwa woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa, kapena kwa owombeza. Musamawafunefune kuti angakuyipitseni. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.
32 “ ‘Muzikhala mwa ulemu pamaso pa munthu wachikulire, ndipo muzichitira ulemu munthu wokalamba. Kumeneko ndiye kuopa Mulungu wanu. Ine ndine Yehova.
33 “ ‘Pamene mlendo akhala nanu m’dziko mwanu, musamuzunze.
34 Mlendo amene akhala nanu akhale ngati mmodzi mwa mbadwa zanu. Mumukonde monga momwe mumadzikondera inu nomwe. Paja inu munali alendo m’dziko la Igupto. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.
35 “ ‘Musamachite za chinyengo poweruza mlandu, kapena poyeza
utali, kulemera ngakhalenso kuchuluka kwa zinthu. 36 Miyeso ya sikelo,
miyeso yoyezera kulemera kwa zinthu, miyeso yotchedwa efa ndi miyeso yotchedwa hini zikhale zolungama. Ine ndine Yehova, Mulungu wanu amene ndinakutulutsani ku dziko la Igupto.
37 “ ‘Choncho muzisunga malangizo ndi malamulo angawa ndi kuwatsatira. Ine ndine Yehova.’ ”

# 20

*Zilango za Tchimo*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 “Uza Aisraeli kuti, ‘Mwisraeli aliyense
kapena mlendo aliyense wokhala mu Israeli wopereka mwana wake
kwa Moleki ayenera kuphedwa. Anthu a m’dera lakelo amuphe ndi
miyala. 3 Munthu ameneyo ndidzamufulatira ndi kumuchotsa pakati
pa anzake.’ Popereka mwana wake kwa Moleki, wadetsa malo anga
wopatulika ndi kuyipitsa dzina langa loyera. 4 Ngati anthu a m’deralo
achita ngati sakumuona munthuyo pamene akupereka mwana wake kwa
Moleki ndi kusamupha, 5 Ineyo ndidzamufulatira pamodzi ndi banja
lake. Ndidzawachotsa pakati pa anthu anzawo onse amene anamutsatira, nadziyipitsa okha popembedza Moleki.”
6 “ ‘Ngati munthu adzapita kwa woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa kapena kwa owombeza, nadziyipitsa powatsatira iwowo, Ine ndidzamufulatira ndi kumuchotsa pakati pa anthu anzake.
7 “ ‘Chifukwa chake dzipatuleni ndi kukhala woyera popeza Ine ndine
Yehova Mulungu wanu. 8 Ndipo sungani malangizo anga ndi kuwatsata.
Ine ndine Yehova amene ndimakuyeretsani.
9 “ ‘Munthu aliyense amene atemberera abambo ake kapena amayi ake ayenera kuphedwa. Magazi ake adzakhala pamutu pake chifukwa iye watemberera abambo kapena amayi ake.

10 “ ‘Ngati munthu wachita chigololo ndi mkazi wa mnzake, mwamu-
nayo pamodzi ndi mkaziyo ayenera kuphedwa.
11 “ ‘Ngati munthu agonana ndi mkazi wa abambo ake, wachititsa
manyazi abambo ake. Munthuyo pamodzi ndi mkaziyo ayenera
kuphedwa. Magazi awo adzakhala pa mitu pake.
12 “ ‘Ngati munthu agonana ndi mkazi wa mwana wake, awiriwo
ayenera kuphedwa. Iwo achita chinthu chonyansa kwambiri. Magazi awo
adzakhala pa mitu pawo.
13 “ ‘Ngati munthu agonana ndi mwamuna mnzake ngati akugonana ndi
mkazi, ndiye kuti onsewo achita chinthu cha manyazi. Choncho aphedwe.
Magazi awo adzakhala pa mitu pawo.
14 “ ‘Ngati munthu akwatira mkazi, nakwatiranso amayi ake, chimene-
cho ndi chinthu choyipa kwambiri. Mwamunayo pamodzi ndi akaziwo
ayenera kutenthedwa pa moto kuti chinthu choyipa chotere chis-
apezekenso pakati panu.
15 “ ‘Ngati mwamuna agonana ndi nyama, iye ayenera kuphedwa, ndipo
muyeneranso kupha nyamayo.
16 “ ‘Ngati mkazi agonana ndi nyama, aphedwe pamodzi ndi nyamayo.
Mkaziyo ndi nyamayo ayenera kuphedwa, ndipo magazi awo adzakhala
pa mitu pawo.
17 “ ‘Ngati munthu akakwatira mlongo wake, mwana wamkazi wa
abambo ake, kapena mwana wamkazi wa amayi ake, ndipo iwo
n’kugonana, ndiye kuti achita chinthu chochititsa manyazi. Onse awiri
ayenera kuchotsedwa pa gulu la abale awo. Tsono popeza munthuyo
wachititsa manyazi mlongo wake, adzayenera kulandira chilango.
18 “ ‘Ngati munthu agonana ndi mkazi pa nthawi yake yosamba, ndiye
kuti wavula msambo wake, ndipo mkaziyo wadzivulanso. Onse awiri
achotsedwe pakati pa anthu anzawo.
19 “ ‘Musagonane ndi mchemwali wa amayi anu kapena abambo anu,
pakuti kutero ndi kuchititsa manyazi m’bale wanu. Nonse mudzalipira
mlandu wanu.
20 “ ‘Ngati munthu agonana ndi azakhali ake, munthuyo wachititsa
manyazi a malume ake. Onse adzalipira mlandu wawo. Onsewo adzafa
wopanda mwana.
21 “ ‘Munthu akakwatira mkazi wa mchimwene wake ndiye kuti wachita
chinthu chonyansa. Wachititsa manyazi m’bale wakeyo. Onse awiriwo
adzakhala wopanda mwana.
22 “ ‘N’chifukwa chake muzisunga malangizo anga onse ndi malamulo
anga ndipo muwatsatire kuti ku dziko limene Ine ndikupita nanu kuti
mukakhalemo lisakakusanzeni. 23 Musatsanzire miyambo ya mitundu
ya anthu imene ndi kuyipirikitsa inu mukufika. Chifukwa iwo anachita
zinthu zonsezi, ndipo Ine ndinanyansidwa nawo. 24 Koma Ine ndi-
nakuwuzani kuti, ‘Mudzatenga dziko lawo. Ine ndidzakupatsani dzikolo
kuti likhale cholowa chanu, dziko loyenda mkaka ndi uchi.’ Ine ndine
Yehova Mulungu wanu amene ndakupatulani pakati pa mitundu yonse ya
anthu.
25 “ ‘Chifukwa chake muzisiyanitsa pakati pa nyama zoyeretsedwa
ndi nyama zodetsedwa ndiponso pakati pa mbalame zoyeretsedwa ndi
mbalame zodetsedwa. Musadzidetse pakudya nyama iliyonse kapena
mbalame, kapena chilichonse chimene chimakwawa pansi, chimene Ine
ndachipatula kuti chikhale chodetsedwa kwa inu. 26 Muzikhala woyera

pamaso panga chifukwa Ine Yehova, ndine woyera ndipo ndakupatulani
pakati pa anthu a mitundu yonse kuti mukhale anthu anga.
27 " 'Mwamuna kapena mkazi woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa
kapena wanyanga pakati panu ayenera kuphedwa. Muwagende ndi
miyala, ndipo magazi awo adzakhala pa mitu pawo.' "

# 21

*Malamulo a Ansembe*

1 Yehova anawuza Mose kuti, "Yankhula ndi ansembe, ana a Aaroni,
ndipo uwawuze kuti, 'Wansembe asadzidetse pokhudza munthu wakufa
pakati pa abale ake. 2 Koma akhoza kukhudza thupi lakufa la amayi
ake, abambo ake, mwana wake wamwamuna, mwana wake wamkazi,
mchimwene wake, 3 kapena mlongo wake wosakwatiwa amene amadalira
iye chifukwa sanakwatiwe. Iye akhoza kudzidetsa pokhudza thupi lakufa
la mchemwali wake wosakwatiwa yekha. 4 Koma wansembe asadzidetse
chifukwa cha anthu amene ali nawo pa ubale obwera chifukwa cha
ukwati.
5 " 'Ansembe asamete tsitsi kumutu kwawo kapena m'mphepete mwa
ndevu zawo, kapenanso kudzichekacheka pa thupi lawo. 6 Ayenera
kukhala oyera pamaso pa Mulungu wawo ndipo asachititse manyazi dzina
la Mulungu wawo. Popeza amapereka nsembe zotentha pa moto kwa
Yehova, chakudya cha Mulungu wawo, iwo azikhala woyera.
7 " 'Asakwatire akazi amene adzidetsa ndi chiwerewere kapena akazi
amene amuna awo awasudzula, chifukwa ansembe ndi oyera pamaso pa
Mulungu wawo. 8 Iwo akhale oyera chifukwa amapereka nsembe kwa
Mulungu wanu. Muziwaona kuti ndi oyera, popeza Ine Yehova amene
ndimawayeretsa ndine woyera, nawonso akhale oyera.
9 " 'Ngati mwana wamkazi wa wansembe adziyipitsa pochita zachi-
werewere, ndiye kuti iye akuchititsa manyazi abambo ake; mwanayo
atenthedwe pa moto.
10 " 'Munthu amene ali mkulu wa ansembe pakati pa abale ake,
amene anamudzoza pomutsanulira mafuta pamutu pake, ndiponso amene
anapatulidwa pomuveka zovala zaunsembe, asalekerere tsitsi lake kapena
kung'amba zovala zake kusonyeza kuti ali pa chisoni. 11 Asalowe
m'nyumba mmene muli munthu wakufa ngakhale womwalirayo ndi
amayi ake kapena abambo ake. 12 Asadzidetse potulukira kunja kwa malo
opatulika popeza mafuta womupatula kukhala wansembe ali pamutu
pake. Ine ndine Yehova.
13 " 'Iye akwatire namwali wosadziwa mwamuna. 14 Asakwatire mkazi
wamasiye, mkazi wosudzulidwa, kapena mkazi wachiwerewere, koma
akwatire namwali wosadziwa mwamuna pakati pa anthu a mtundu wake,
15 kuti mtundu wake usakhale wodetsedwa pakati pa abale popeza ndine
Yehova, amene ndimamuyeretsa.' "
16 Yehova anawuza Mose kuti, 17 "Muwuze Aaroni kuti, 'Munthu aliyense
mwa zidzukulu zake ku mibado yawo yonse ikubwera akakhala ndi
chilema asabwere kudzapereka nsembe kwa Mulungu wake. 18 Munthu
aliyense wachilema motere: munthu wakhungu kapena wolumala
miyendo, munthu wolumala nkhope kapena waziwalo zambiri, 19 munthu
wa phazi lolumala kapena dzanja lolumala, 20 kapena munthu wokhota
msana kapena wamfupi kwambiri, kapena wolumala maso, munthu
wa nthenda yonyerenyetsa, kapena wamphere, kapenanso wophwanyika

mavalo, sayenera kusendera pafupi. 21 Mdzukulu aliyense wa Aaroni
wansembe, amene ali ndi chilema asadzayandikire kukapereka nsembe
zopsereza kwa Yehova. Popeza kuti ali ndi chilema, asayandikire kudza-
pereka nsembe ya chakudya kwa Mulungu wake. 22 Koma iye angathe
kudya chakudya chopatulika kwambiri chija, ngakhalenso chakudya
chotsala pa nsembe zopatulika. 23 Koma chifukwa cha kulumala kwake,
sayenera kuyandikira katani kapena kufika pa guwa kuti angadetse malo
anga wopatulika. Ine ndine Yehova, amene ndimawayeretsa.' "

24 Choncho Mose anawuza Aaroni ndi ana ake pamodzi ndi Aisraeli onse
zimenezi.

# 22

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Uza Aaroni ndi ana ake kuti azilemekeza
zinthu zopatulika zimene Aisraeli azipereka kwa Ine, kuti asayipitse dzina
langa loyera. Ine ndine Yehova.

3 "Uwawuze kuti ngati wina aliyense mwa zidzukulu zawo m'mibado
yonse imene ikubwera adzayandikira zinthu zopatulika zimene ana a
Israeli apereka kwa Yehova, ali wodetsedwa, ameneyo achotsedwe pamaso
pa Yehova. Ine ndine Yehova.

4 "Munthu aliyense mwa zidzukulu za Aaroni amene ali ndi khate
kapena amatulutsa zoyipa m'thupi mwake, asadye zinthu zopatulika
mpaka atayeretsedwa. Wansembe angakhale wodetsedwa atakhudzana
ndi chinthu chimene chadetsedwa ndi chinthu chakufa kapena kukhudza
munthu amene wataya umuna, 5 kapena kukhudza chilichonse chok-
wawa chomwe chimadetsa munthu, kapena kukhudza munthu amene
angamudetse, kapenanso kukhudza kanthu kena kalikonse kodetsedwa.
6 Tsono ngati wansembe angakhudze chilichonse mwa zimenezi ndiye kuti
adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo. Asadye chopereka chilichonse
chopatulika mpaka atasamba thupi lake lonse. 7 Munthuyo adzakhala
woyeretsedwa pamene dzuwa lalowa, ndipo angathe kudya chopereka
chopatulikacho popeza ndi chakudya chake. 8 Wansembe sayenera
kudya chinthu chofa chokha kapena chojiwa ndi chirombo kuopa kuti
angadzidetse ndi chakudyacho. Ine ndine Yehova.

9 " 'Choncho ansembe azisunga malamulo angawa kuti asapezeke
wolakwa ndi kufa chifukwa chopeputsa malamulowa. Ine ndine Yehova,
amene ndimawayeretsa.

10 " 'Aliyense amene si wabanja la wansembe, kaya ndi mlendo
wa wansembe, kapena wantchito wake, asadye chopereka chopatu-
lika. 11 Koma kapolo amene wagulidwa ndi ndalama kapena kubad-
wira m'banja la wansembe angathe kudya chakudya cha wansembeyo.
12 Mwana wamkazi wa wansembe amene wakwatiwa ndi munthu amene
si wansembe, asadyeko nsembe zopatulikazo. 13 Koma mwana wamkazi
wa wansembe amene ali wamasiye kapena wosudzulidwa, ndipo alibe
mwana, komanso anabwerera ku nyumba ya abambo ake monga pa
nthawi ya utsikana wake, angathe kudya chakudya cha abambo ake.
Mlendo asadye chakudya chopatulika.

14 " 'Ngati munthu wina aliyense adya chopereka chopatulika
mosadziwa, munthuyo amubwezere wansembe chinthu chopatulikacho
ndipo awonjezerepo limodzi la magawo asanu a chinthucho. 15 Choncho
ansembe asayipitse zopereka zopatulika za Aisraeli zimene apereka kwa
Yehova 16 ndipo asachimwitse ndi kupalamulitsa Aisraeli powalola kudya
zakudya zawo zopatulika. Ine ndine Yehova amene ndimawayeretsa.' "

*Nsembe Zosavomerezeka*

17 Yehova anawuza Mose kuti, 18 “Yankhula ndi Aaroni, ana ake pamodzi
ndi Aisraeli onse, ndipo uwawuze kuti, ‘Ngati wina aliyense wa inu,
Mwisraeli kapena mlendo amene akukhala mu Israeli abwera ndi mphatso
ya nsembe yopsereza kwa Yehova, kupereka chimene analumbira kapena
kuti ikhale nsembe yaufulu, 19 ndiye kuti abwere ndi ng’ombe yayimuna,
nkhosa yayimuna kapena mbuzi yayimuna. Izi zikhale zopanda chilema
kuti zilandiridwe. 20 Musapereke nyama iliyonse yokhala ndi chilema
chifukwa sidzalandiridwa m’malo mwanu. 21 Pamene wina aliyense
abweretsa ng’ombe kapena nkhosa kuti ikhale nsembe yachiyanjano kwa
Yehova, kukwaniritsa zimene analumbira kapena kuti ikhale nsembe
yaufulu, nyamayo iyenera kukhala yangwiro ndi yopanda chilema kuti
ilandiridwe. 22 Musapereke kwa Yehova nyama zakhungu, zovulala
kapena zolumala, kapena nyama zimene zikutulutsa mafinya m’thupi
mwake, kapena zimene zili ndi nthenda yonyerenyetsa, kapena zimene
zili ndi mphere. Nyama zotere musaziyike pa guwa kuti zikhale nsembe
yopsereza kwa Yehova. 23 Koma mungathe kupereka ng’ombe yayimuna
kapena nkhosa imene ili ndi chiwalo chachitali kapena chachifupi kukhala
nsembe yaufulu. Koma simungayipereke ngati nsembe yoperekera
zimene munalumbirira chifukwa sidzalandiridwa. 24 Nyama iliyonse
imene mavalo ake ndi onyuka kapena ophwanyika, ong’ambika kapena
oduka, musamayipereke kwa Yehova m’dziko lanu. 25 Ndipo musalandire
nyama zotere kuchokera kwa mlendo ndi kuzipereka kukhala zakudya za
Mulungu wanu. Zimenezi sizidzalandiridwa m’malo mwanu chifukwa zili
ndi chilema ndipo ndi zolumala.’ ”

26 Yehova anawuza Mose kuti, 27 “Pamene mwana wang’ombe, mwana
wankhosa kapena mwana wambuzi wabadwa, akhale ndi make kwa
masiku asanu ndi awiri. Kuyambira tsiku lachisanu ndi chitatu mpaka
m’tsogolo mwake, angathe kulandiridwa kuti akhale nsembe yopsereza
ya kwa Yehova. 28 Musaphe ng’ombe kapena nkhosa pamodzi ndi mwana
wake tsiku limodzi. Muyidye pa tsiku lomwelo; musasiyeko ina mpaka
mmawa. Ine ndine Yehova.

29 “Pamene mupereka nsembe yoyamika kwa Yehova, muyipereke
mwakufuna kwanu mu njira yoti ilandiridwe m’malo mwanu. 30 Muyidye
pa tsiku lomwelo, wosasiyako ina mpaka mmawa. Ine ndine Yehova.

31 “Choncho sungani malamulo anga ndi kuwatsatira. Ine ndine
Yehova. 32 Musanyoze dzina langa loyera. Koma lilemekezedwe pakati
pa Aisraeli. Ine ndine Yehova amene ndimakuyeretsani 33 ndipo ndine
amene ndinakutulutsani mu Igupto kuti ndikhale Mulungu wanu. Ine
ndine Yehova.”

## 23

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 “Yankhula ndi Aisraeli ndipo uwawuze
kuti, ‘Awa ndi masiku anga osankhika a chikondwerero, masiku osankhika
olemekeza Yehova amene uyenera kulengeza kuti akhale masiku opatulika
a misonkhano.

*Za Sabata*

3 “ ‘Pa masiku asanu ndi limodzi muzigwira ntchito, koma tsiku
lachisanu ndi chiwiri ndi Sabata lopuma, tsiku la msonkhano wopatulika.
Kulikonse kumene inu mukukhala musamagwire ntchito iliyonse tsiku
limeneli popeza ndi tsiku la Sabata la Yehova.

### *Za Paska ndi za Buledi Wopanda Yisiti*

4 “ ‘Awa ndiwo masiku osankhidwa a zikondwerero za Yehova, masiku
woyera a misonkhano amene muti mudzalengeze pa nthawi yake:
5 Chikondwerero cha Paska chiziyamba madzulo a tsiku la 14 la mwezi
woyamba. 6 Tsiku la 15 la mwezi womwewo ndi tsiku lolemekeza Yehova
ndipo muziyamba Chikondwerero cha Buledi Wopanda Yisiti. Muzidya
buledi wopanda yisiti kwa masiku asanu ndi awiri. 7 Pa tsiku loyamba
muzichita msonkhano wopatulika. Musamagwire ntchito iliyonse. 8 Pa
masiku asanu ndi awiri muzipereka nsembe yopsereza kwa Yehova. Ndipo
tsiku lachisanu ndi chiwiri muzikhala ndi msonkhano wopatulika ndipo
musamagwire ntchito yolemetsa.’ ”

### *Za Zipatso Zoyambirira Kucha*

9 Yehova anawuza Mose kuti, 10 “Yankhula ndi Aisraeli ndipo uwawuze
kuti, ‘Mukakalowa m’dziko limene ndikukupatsanilo ndi kukolola za
m’minda mwanu, mudzabwere kwa wansembe ndi mtolo wa tirigu
woyambirira kucha wa m’minda mwanu. 11 Wansembeyo auweyule
mtolowo pamaso pa Yehova kotero mtolowo udzalandiridwa m’malo
mwanu. Wansembe auweyule tsiku lotsatana ndi la Sabata. 12 Pa
tsiku limene muweyula mtolowo, muperekenso mwana wankhosa wa
mwamuna wa chaka chimodzi, wopanda chilema kuti akhale nsembe
yopsereza ya kwa Yehova. 13 Chopereka chachakudya chake chikhale cha
makilogalamu awiri a ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta kuti chikhale
nsembe yopsereza yopereka kwa Yehova, ya fungo lokoma. Ndipo
chopereka cha chakumwa chake chikhale vinyo wa malita anayi ndi theka.
14 Musadye buledi aliyense kapena tirigu wokazinga, kapena wamuwisi
mpaka tsiku limene mwabwera ndi chopereka ichi kwa Mulungu wanu.
Limeneli ndi lamulo lamuyaya pa mibado yanu yonse, kulikonse kumene
mukakhale.

### *Chikondwerero cha Masabata*

15 “ ‘Kuyambira tsiku lotsatana ndi la Sabata lija, tsiku limene munab-
wera ndi mtolo wa nsembe yoweyula, muziwerenga masabata asanu
ndi awiri athunthu. 16 Ndiye kuti muwerenge masiku makumi asanu
kuchokera pa tsiku lotsatana ndi Sabata la chisanu ndi chiwiri, ndipo
kenaka mupereke nsembe ya tirigu watsopano kwa Yehova. 17 Kuchokera
kulikonse kumene mukukhala, mubwere pamaso pa Yehova ndi buledi
muwiri wa ufa wosalala wa makilogalamu awiri, ophikidwa ndi yisiti kuti
akhale nsembe yoweyula ya zakudya zoyamba kucha. 18 Pamodzi ndi
buledi yu muperekenso ana ankhosa aamuna asanu ndi awiri, aliyense
akhale wa chaka chimodzi ndi wopanda chilema. Pakhalenso ng’ombe
yaying’ono yayimuna ndi nkhosa zazimuna ziwiri. Zimenezi zidzakhala
nsembe zopsereza zopereka kwa Yehova pamodzi ndi nsembe za zakudya
ndi nsembe za zakumwa. Zonsezi zikhale nsembe zopsereza za fungo
lokomera Yehova. 19 Kenaka mupereke mbuzi imodzi yayimuna kuti
ikhale nsembe yopepesera machimo ndiponso ana ankhosa awiri, aliyense
wa chaka chimodzi kuti akhale nsembe yachiyanjano. 20 Wansembe
aweyule ana ankhosa awiriwo pamaso pa Yehova monga nsembe
yoweyula, pamodzi ndi buledi wa tirigu woyambirira kucha. Zimenezi
ndi zopereka zopatulika za Yehova zopatsidwa kwa ansembe. 21 Pa
tsiku lomwelo mulengeze za msonkhano wopatulika ndipo musagwire
ntchito zolemetsa. Limeneli ndi lamulo lamuyaya pa mibado yanu yonse,
kulikonse kumene mukakhale.

22 " 'Pamene mukukolola zinthu m'munda mwanu, musakolole munda
wanu mpaka m'malire mwenimweni, ndipo musatole khunkha lake.
Zimenezo musiyire anthu osauka ndi alendo. Ine ndine Yehova Mulungu
wanu.' "

*Chikondwerero cha Malipenga*

23 Yehova anawuza Mose kuti, 24 "Uza Aisraeli kuti, 'Tsiku loyamba
la mwezi wachisanu ndi chiwiri, likhale tsiku lopumula, la msonkhano
wopatulika, mulilengeze poyimba lipenga. 25 Musagwire ntchito zolemetsa
koma mupereke nsembe yopsereza kwa Yehova.' "

*Tsiku Lopepesera Machimo*

26 Yehova anawuza Mose kuti, 27 "Tsiku lakhumi la mwezi wachisanu
ndi chiwiri ndi tsiku lochita Mwambo Wopepesera Machimo. Muzichita
msonkhano wopatulika. Muzidzichepetsa pamaso pa Yehova ndi ku-
pereka nsembe zopsereza kwa Yehova. 28 Tsiku limeneli musamagwire
ntchito chifukwa ndi tsiku la Mwambo Wopepesera Machimo, kupepesera
machimo anu pamaso pa Yehova Mulungu wanu. 29 Munthu aliyense
amene sasala zakudya pa tsiku limeneli ayenera kuchotsedwa pakati
pa anthu a mtundu wake. 30 Aliyense wogwira ntchito tsiku limeneli
ndidzamuwononga pakati pa anthu a mtundu wake. 31 Inu musadzagwire
ntchito iliyonse. Limeneli ndi lamulo lamuyaya pa mibado yanu yonse,
kulikonse kumene mukakhale. 32 Limeneli kwa inu ndi tsiku la Sabata
lopumula, ndipo muyenera kusala zakudya. Kuyambira madzulo a tsiku
lachisanu ndi chinayi la mwezi mpaka madzulo ena otsatirawo muzisunga
tsikulo ngati Sabata lanu."

*Chikondwerero cha Misasa*

33 Yehova anawuza Mose kuti, 34 "Uwawuze Aisraeli kuti pa masiku
asanu ndi awiri kuyambira pa tsiku la 15 la mwezi wachisanu ndi chiwiri
pazikhala Chikondwerero cha Misasa cholemekeza Yehova. 35 Tsiku loy-
amba ndi la msonkhano wopatulika, musagwire ntchito zolemetsa. 36 Pa
masiku asanu ndi awiri muzipereka nsembe zopsereza kwa Yehova. Ndipo
pa tsiku lachisanu ndi chitatu muzikhala ndi msonkhano wopatulika ndipo
muzipereka nsembe yopsereza kwa Yehova. Kumeneku ndi kutsekera kwa
msonkhano waukulu. Musagwire ntchito zolemetsa.

37 (" 'Amenewa ndi masiku osankhika a chikondwerero cha Yehova,
amene muziwalengeza kuti ndi nthawi ya msonkhano wopatulika. Masiku
amenewa muzipereka nsembe zopsereza, nsembe za chakudya, nsembe
zanyama ndi zopereka zachakumwa za tsiku ndi tsiku. 38 Zopereka
zimenezi ndi zowonjezera pa zopereka za Yehova za pa Sabata, zopereka
zanu zolumbira ndiponso mphatso zanu zaufulu zopereka kwa Yehova.)

39 " 'Choncho kuyambira pa tsiku la 15 la mwezi wachisanu ndi chiwiri,
mutakolola zinthu m'munda mwanu, muchite chikondwerero cha Yehova
kwa masiku asanu ndi awiri. Tsiku loyamba ndi tsiku lopumula, ndipo
tsiku lachisanu ndi chitatu ndi lopumulanso. 40 Pa tsiku loyamba
muzitenga zipatso zabwino kwambiri zothyola m'mitengo, nthambi za
kanjedza, nthambi zazikulu za mitengo ya masamba ambiri, ndi za
misondozi yakumtsinje, ndipo muzikondwera pamaso pa Yehova Mulungu
wanu kwa masiku asanu ndi awiri. 41 Chaka chilichonse muzichita
chikondwerero cha Yehova kwa masiku asanu ndi awiri. Limeneli ndi
lamulo lamuyaya pa mibado yanu yonse. Muzichita chikondwerero
chimenechi mwezi wachisanu ndi chiwiri. 42 Muzikhala m'misasa

masiku asanu ndi awiri. Onse amene ali mbadwa m'dziko la Israeli
azikhala m'misasa 43 kuti zidzukulu zanu zidzadziwe kuti ndine amene
ndinakhazika Aisraeli m'misasa nditawatulutsa ku Igupto. Ine ndine
Yehova Mulungu wanu.' "

44 Choncho Mose analengeza kwa Aisraeli masiku osankhika a zikondw-
erero za Yehova.

# 24

### *Mafuta ndi Buledi wa Pamaso pa Yehova*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Lamula Aisraeli kuti akupatse mafuta
anyale, a olivi wabwino kwambiri kuti nyalezo ziziyaka nthawi zonse.
3 Kunja kwa nsalu yotchinga Bokosi la Chipangano, m'chihema cha
msonkhano, Aaroni azionetsetsa kuti nyale ikukhala chiyakire pamaso pa
Yehova kuyambira madzulo mpaka mmawa, nthawi zonse. Limeneli ndi
lamulo lamuyaya pa mibado yonse. 4 Aaroni ayatse nyale zimene zili pa
choyikapo nyale chagolide wabwino kwambiri kuti zikhale zoyaka nthawi
zonse pamaso pa Yehova.

5 "Mutenge ufa wosalala ndipo muphike makeke khumi ndi awiri ndipo
keke iliyonse ikhale ya ufa wa makilogalamu awiri. 6 Muwayike pa tebulo
la golide wabwino kwambiri pamaso pa Yehova m'mizere iwiri. Mzere
uliwonse ukhale wa makeke asanu ndi imodzi. 7 Pa mzere uliwonse
muyikepo lubani wafungo lokoma kuti pamodzi ndi bulediyo akhale
wachikumbutso cha nsembe yopsereza yopereka kwa Yehova. 8 Sabata ndi
sabata nthawi zonse Aaroni aziyika makeke amenewa pamaso pa Yehova
m'malo mwa Aisraeli onse kuti akhale pangano lamuyaya. 9 Chakudyacho
ndi cha Aaroni ndi ana ake ndipo azidyera ku malo wopatulika chifukwa
kwa iye chakudyacho ndi chopatulika kwambiri chochokera pa chopereka
chopsereza cha Yehova."

### *Woyankhula Monyoza Mulungu Aphedwa ndi Miyala*

10 Tsiku lina munthu wina wamwamuna amene amayi ake anali
Mwisraeli koma abambo ake anali Mwigupto anapita kwa Aisraeli ndipo
anakangana ndi Mwisraeli wina ku msasa. 11 Munthu uja ananyoza dzina
la Yehova ndi kulitemberera. Choncho anabwera naye kwa Mose. Dzina la
amayi ake linali Selomiti, mwana wa Dibiri, wa fuko la Dani. 12 Anamuyika
m'ndende mpaka atadziwa bwino chofuna cha Yehova.

13 Ndipo Yehova anawuza Mose kuti, 14 "Pita naye kunja kwa msasa
munthu wotembererayo. Onse amene anamumva akutemberera asanjike
manja awo pamutu pake ndipo gulu lonse la anthu limugende miyala.
15 Choncho uza Aisraeli kuti, 'Aliyense wotemberera Mulungu wake
alangidwe. 16 Aliyense wonyoza dzina la Yehova, mlendo ngakhale
mbadwa, aphedwe. Gulu lonse la anthu limuponye miyala.

17 " 'Ngati munthu wina aliyense achotsa moyo wa munthu mnzake,
munthuyo ayenera kuphedwa. 18 Aliyense wopha chiweto cha mnzake
ayenera kulipira china. Moyo kulipa moyo. 19 Ngati munthu avulaza
mnzake, nayenso amuchite zomwe wachitira mnzakeyo: 20 kuthyola fupa
kulipira kuthyola fupa, diso kulipira diso, dzino kulipira dzino. Monga
momwe anavulazira mnzake, amuvulaze chimodzimodzinso. 21 Aliyense
wopha chiweto cha mnzake, alipire chiweto china, koma aliyense wopha
munthu ayenera kuphedwa. 22 Lamulo la mlendo ndi mbadwa ndi limodzi
lomweli. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.' "

[23] Pamenepo Mose anawuza Aisraeli zimenezi, ndipo iwo anatulutsira
munthu wotembererayo kunja kwa msasa ndi kumugenda miyala. Ais-
raeli anachita zimene Yehova analamula Mose.

# 25

*Za Chaka Chopumula*

[1] Yehova anawuza Mose pa phiri la Sinai kuti, [2] "Yankhula ndi Aisraeli
ndipo uwawuze kuti, 'Mukadzalowa m'dziko limene ndikukupatsani,
nthakayo iyenera kumakasunga Sabata la Yehova. [3] Pa zaka zisanu ndi
chimodzi muzikalima minda yanu, ndipo kwa zaka zisanu ndi chimodzi
muzikasadza mitengo yanu ya mpesa ndi kuthyola zipatso zake. [4] Koma
chaka chachisanu ndi chiwiri ndi chaka choti nthaka ipume, chaka cha
Sabata la Yehova. Musalime m'minda yanu kapena kusadza mitengo
yanu ya mpesa. [5] Musakolole zimene zinamera zokha m'munda mwanu.
Musakakolole kapena kuthyola mphesa za m'mitengo imene simunasadze.
Chaka chimenechi n'choti nthaka ipumule. [6] Chaka chimene nthakayo
ipumula mudzakhala ndi chakudya chokwanira inuyo, akapolo anu
aamuna ndi aakazi, antchito ndi alendo okhala nanu. [7] Ziweto zanu
pamodzi ndi nyama za m'dziko lanu zizidzadya zipatso za m'nthaka.

*Chaka Chokondwerera Zaka Makumi Asanu*

[8] " 'Muzichotsera Masabata asanu ndi awiri a zaka, ndi kuchulukitsa
zaka zisanu ndi ziwiri kasanu ndi kawirinso kuti Masabata asanu ndi
awiri a zakawo akwane zaka 49. [9] Ndipo pa tsiku la khumi la mwezi
wachisanu ndi chiwiri mulize lipenga mofuwula. Tsiku lochita mwambo
wopepesera machimo muziliza lipenga m'dziko lanu lonse. [10] Mupatule
chaka cha makumi asanu, ndipo mulengeze kuti pakhale ufulu m'dziko
lonse kwa onse amene ali m'menemo. Kwa inu chakachi chidzakhala
choyimba lipenga la chikondwerero. Aliyense wa inu adzayenera
kubwerera pa munda wake, ndipo aliyense wa inu adzabwerera ku
fuko lake. [11] Kwa inu chakachi chidzakhaladi chaka choyimba lipenga
kukondwerera zaka makumi asanu. Pa chaka chimenechi musadzale
kanthu ndipo musakolole mbewu zomera zokha kapenanso kuthyola
mphesa pa mitengo yosasadzira. [12] Chimenechi ndi chaka chokondwerera
zaka makumi asanu. Choncho chikhale chaka chopatulika kwa inu.
Muzidya zokhazo zimene zakololedwa m'minda.

[13] " 'Chaka chimenechi ndi choliza lipenga, kukondwerera zaka makumi
asanu, ndipo aliyense abwerere pa malo ake.

[14] " 'Ngati unagulitsa kapena kugula malo ako kwa mnzako wa
m'dzikomo, pasakhale kuchenjeretsana. [15] Ugule kwa mnzako potsata
chiwerengero cha zaka zimene zatha kuyambira pa chikondwerero cha
chaka cha makumi asanu chapita. Ndipo mnzakoyo akugulitse potsata chi-
werengero cha zaka zokolola zomwe zatsala. [16] Zaka zikakhala zochuluka,
uwonjezere mtengo, ndipo zaka zikakhala zochepa, uchepetse mtengo,
pakuti chimene iye akukugulitsa ndi zaka zokolola. [17] Musachenjeretsane
koma muope Mulungu wanu. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.

[18] " 'Tsatirani malangizo anga ndipo mverani mosamala malamulo
anga ndipo mudzakhala m'dzikomo mwamtendere. [19] Ndipo nthaka
idzakupatsani zipatso zake. Mudzadya mpaka kukhuta ndiponso mudza-
khala m'dzikomo mwamtendere. [20] Mwina n'kafunsa kuti, 'Kodi chaka
chachisanu ndi chiwiri tidzadya chiyani ngati sitidzala kapena kukolola
mbewu zathu?' [21] Ine ndidzatumiza madalitso ambiri chaka chachisanu

ndi chimodzi moti nthaka yanu idzabala zinthu zokwanira kudya zaka
zitatu. 22 Pamene mukudzala chaka chachisanu ndi chitatu, muzidzadya
chakudya chogonera ndipo mudzapitirira kudya mpaka nthawi yokolola
m'chaka chachisanu ndi chinayi.

23 " 'Malo asagulitsidwe mpaka muyaya chifukwa dzikolo ndi langa. Inu
ndinu alendo okhala ndi Ine. 24 Malo onse amene ali m'manja mwanu
mudzalole kuti amene anakugulitsani awawombole.

25 " 'Ngati Mwisraeli mnzanu wasauka nagulitsako gawo lina la malo
ake, m'bale wake wapaphata abwere kudzawombola malo amene m'bale
wakeyo wagulitsa. 26 Koma ngati munthuyo alibe wachibale woti
n'kuwombola malowo koma pambuyo pake iye mwini n'kulemera ndi ku-
peza zokwanira kuwombolera, awombole malowo. 27 Awerengerane zaka
kuyambira pamene anagulitsa mundawo ndipo amubwezere amene anag-
ulayo ndalama zimene akanayenera kuzipereka mpaka chaka chokondw-
erera zaka makumi asanu. Atatero angathe kubwerera pa malo ake.
28 Koma ngati sakhala nazo zokwanira kuti amubwezere amene anagula
malowo, gawo limene anagulitsalo lidzakhala m'manja mwa munthu
amene anagulayo mpaka chaka chokondwerera zaka makumi asanu.
Malowo adzabwezedwa chaka chimenechi, ndipo iye adzatha kubwerera
pa malo ake.

29 " 'Ngati munthu agulitsa nyumba ya mu mzinda umene uli mu
linga, angathe kuyiwombola nyumbayo chisanathe chaka chathunthu
chigulitsire. Mu nthawi imeneyi wogulitsayo atha kuyiwombola. 30 Ngati
nyumbayo siwomboledwa chisanathe chaka chimodzicho, nyumbayo
idzakhala ya amene anagulayo ndi zidzukulu zake mpaka muyaya.
Sidzabwezedwanso kwa mwini wake m'chaka chokondwerera zaka
makumi asanu. 31 Koma nyumba za m'mizinda yosazingidwa ndi linga
ziwomboledwe monga mmene achitira ndi minda ya m'dzikomo.

32 " 'Alevi ali ndi ufulu owombola nyumba zawo za m'midzi yawo
nthawi ina iliyonse. 33 Koma ngati Mlevi sawombola nyumba imene
inagulitsidwa m'mudzi mwake, ndiye kuti idzabwezedwe m'chaka choliza
lipenga pokondwerera zaka makumi asanu, popeza nyumba zimenezi zili
m'midzi ya Alevi ndi yawo pakati pa Aisraeli. 34 Koma malo owetera
ziweto a m'midzi yawoyo sayenera kugulitsidwa. Awa ndi malo awo
mpaka muyaya.

35 " 'Ngati m'bale wako akhala wosauka kuti sangathe kudzisamalira
yekha, umuthandize. Ukhale naye ngati mlendo kapena ngati munthu
amene ukhala naye kwa kanthawi. 36 Usalandire chiwongoladzanja
chilichonse kuchokera kwa iye kapena kuwonjezerapo kanthu kena, koma
uziopa Mulungu kuti m'bale wakoyo akhale nawe. 37 Musakongoze
mnzanu ndalama kuti mulandire chiwongoladzanja, kapena kumugulitsa
chakudya kuti mupeze phindu. 38 Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene
ndinakutulutsani m'dziko la Igupto kuti ndikupatseni dziko la Kanaani ndi
kuti ndikhale Mulungu wanu.

39 " 'Ngati m'bale wanu asauka ndipo adzigulitsa yekha kwa inu,
musamugwiritse ntchito ngati kapolo. 40 Akhale ngati wantchito kapena
ngati mlendo. Akugwirireni ntchito mpaka chaka chokondwerera zaka
makumi asanu. 41 Kenaka iye ndi ana ake achoke, ndipo apite ku fuko
lake ndi kubwerera ku malo a makolo ake. 42 Chifukwa Aisraeli ndi
atumiki anga amene ndinawatulutsa m'dziko la Igupto, asagulitsidwe
ngati akapolo. 43 Musawalamulire mwankhanza koma wopani Mulungu
wanu.

44 “ ‘Kunena za akapolo aamuna ndi aakazi, amenewa mungathe
kuwagula kuchokera kwa mitundu ya anthu imene yakuzungulirani.
45 Mungathenso kugula akapolo kuchokera kwa alendo amene akukhala
nanu kapena kuchokera ku mabanja amene mukukhala nawo amene
ndi mbadwa za m’dziko lanu. Iwowa akhoza kukhala akapolo anu.
46 Akapolowo mungathe kuwasiya m’manja mwa ana anu inu mutafa
kuti akhale cholowa chawo moyo wawo wonse. Koma musawalamulire
mwankhanza Aisraeli anzanu.
47 “ ‘Ngati mlendo kapena munthu amene akukhala nanu kwa kanthawi
kochepa alemera ndipo mmodzi wa abale anu amene akukhala naye
pafupi n’kusauka, nadzigulitsa yekha kwa mlendo amene akukhala pakati
panuyo kapena kwa mmodzi wa fuko la munthu wongokhala pafupi
nayeyo, 48 wodzigulitsayo ali ndi ufulu wowomboledwa. Mmodzi mwa
abale ake angathe kumuwombola: 49 amalume ake kapena mwana wa
amalume ake, kapena wachibale wa mu fuko lake. Kapena ngati iye mwini
alemera, atha kudziwombola yekha. 50 Iye pamodzi ndi munthu amene
anamugulayo awerengerane kuyambira chaka chimene anadzigulitsa
kwa iyeyo mpaka chaka chokondwerera zaka makumi asanu. Mtengo
wodziwombolera ukhale wofanana ndi zakazo. Ndipo nthawi imene anali
ndi mbuye wakeyo iwerengedwe ngati nthawi ya munthu wantchito.
51 Ngati patsala zaka zambiri, iye ayenera kulipira mtengo woposera
umene anamugulira. 52 Ngati kwatsala zaka zochepa kuti ifike nthawi ya
chaka chokondwerera zaka makumi asanu, iye awerengerane ndi mbuye
wake, ndipo apereke ndalama za zowomboledwera molingana ndi zaka
zotsalazo. 53 Azikhala naye ngati wantchito wolembedwa chaka ndi chaka.
Ndipo muonetsetse kuti mbuye wakeyo sakumulamulira mwankhanza.
54 “ ‘Ngakhale munthuyo atapanda kuwomboledwa mwa njira zimenezi,
iye ndi ana ake ayenera kumasulidwa m’chaka chokondwerera zaka
makumi asanu, 55 pakuti Aisraeli ndi atumiki anga. Iwo ndi atumiki anga
amene ndinawatulutsa m’dziko la Igupto. Ine ndine Yehova Mulungu
wanu.

# 26

*Mphotho ya Kumvera*

1 “ ‘Musadzipangire mafano ndipo musayimike chifanizo chosema
kapena mwala woti mudzipembedza. Musayike mwala wosema m’dziko
mwanu kuti muziwugwadira. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.
2 “ ‘Muzisunga Masabata anga ndipo muzilemekeza malo anga wopatu-
lika. Ine ndine Yehova.
3 “ ‘Mukamayenda motsata malangizo anga ndi kumvera mosamalitsa
malamulo anga, 4 ndidzakupatsani mvula pa nyengo yake. Nthaka
yanu idzabala zokolola zake, ndipo mitengo ya m’munda idzabala
zipatso zake. 5 Mudzakhala mukupuntha tirigu mpaka nthawi yothyola
mphesa, ndipo mudzakhala mukuthyola mphesa mpaka nthawi yodzala.
Mudzadya chakudya chanu mpaka kukhuta ndipo mudzakhala m’dziko
lanu mwamtendere.
6 “ ‘Ndidzabweretsa mtendere m’dziko lanu, ndipo muzidzagona
popanda wokuopsezani. Ndidzachotsa nyama zakuthengo zoopsa m’dziko
mwanu, ndipo m’dzikomo simudzakhala nkhondo. 7 Mudzapirikitsa
adani anu, ndipo mudzawagonjetsa ndi lupanga pamaso panu. 8 Anthu
asanu mwa inu adzapirikitsa anthu 100, ndipo anthu 100 mwa inu

adzathamangitsa anthu 10,000, ndipo adani anuwo mudzawagonjetsa ndi lupanga.
9 " 'Ndidzakukumbukirani ndi kukupatsani ana ambiri ndi kukuchuluk-
itsani. Ndidzasunga pangano langa ndi inu. 10 Mudzakhala mukudyabe
chakudya chogonera ndipo mudzachotse chakudyacho m'nkhokwe kuti
mupezemo malo woyika chakudya china chatsopano. 11 Ndidzakhala
pakati panu, ndipo sindidzayipidwa nanu. 12 Ine ndidzayendayenda
pakati panu ndipo ndidzakhala Mulungu wanu. Inu mudzakhala anthu
anga. 13 Ine ndine Yehova Mulungu wanu amene ndinakutulutsani
m'dziko la Igupto kuti musakhalenso akapolo a Aigupto. Ndinadula mipiringidzo ya goli lanu ndi kukuthandizani kuti muziyenda momasuka.

### *Chilango Chakusamvera*

14 " 'Koma mukadzapanda kundimvera ndi kuphwanya malamulo anga
onsewa, 15 ndipo ngati mudzanyoza malangizo anga ndi kunyansidwa ndi
malamulo anga, ndi kulephera kumvera zonse zimene ndakulamulani,
ndi kuswa pangano langa, 16 Ine ndidzakuchitirani izi: ndidzabweretsa zoopsa zadzidzidzi monga chifuwa chachikulu chowondetsa ndiponso malungo amene adzawononga maso ndi kufowoketsa moyo wanu. Mudzangovutika kudzala mbewu zanu chifukwa adani anu adzazidya.
17 Ndidzakufulatirani, kotero kuti adani anu adzakugonjetsani. Odana nanu adzakulamulirani ndipo inu muzidzagothawa popanda wokupirikitsani.
18 " 'Ngati simudzandimvera mutaona zonsezi, ndidzakulanganinso
mochulukitsa kasanu ndi kawiri chifukwa cha kuchimwa kwanu.
19 Ndidzathyola mphamvu zanu zimene mukunyadirazo, ndipo ndidzasandutsa mitambo kuti ikhale yowuma ngati chitsulo, ndiponso nthaka yanu
kuti ikhale ngati mkuwa. 20 Mphamvu zanu zidzapita pachabe chifukwa
nthaka yanu sidzabala kanthu, ngakhale mitengo yake sidzabala zipatso zake.
21 " 'Ngati mudzapitirira kutsutsana nane ndi kukana kundimvera,
ndidzachulukitsa masautso anu kasanu ndi kawiri molingana ndi
machimo anu. 22 Ndidzabweretsa zirombo zolusa pakati panu, ndipo
zidzakulandani ana anu ndi kuwononga ng'ombe zanu. Choncho zidzachepetsa chiwerengero chanu kotero kuti m'njira mwanu simudzapita anthu.
23 " 'Mukadzapanda kutembenukira kwa Ine ngakhale nditakulangani
motere, ndi kumachitabe zotsutsana ndi Ine, 24 Ine mwini ndidzalimbana
nanu, ndipo ndidzakulangani mochulukitsa kasanu ndi kawiri chifukwa
cha machimo anu. 25 Ndipo ndidzabweretsa lupanga pa inu ndi kukulangani chifukwa chophwanya pangano langa. Mukadzasonkhana m'mizinda yanu, ndidzatumiza miliri pakati panu ndipo ndidzakuperekani m'manja
mwa adani anu. 26 Ndikadzachepetsa buledi wanu, akazi khumi adzaphika buledi wawo mu uvuni umodzi, ndipo adzakugawirani bulediyo pang'onopang'ono. Choncho mudzadya koma wosakhuta.
27 " 'Mukadzapanda kundimvera ngakhale nditakulangani motere, ndi
kumatsutsanabe ndi Ine, 28 pamenepo ndidzalimbana nanu mwaukali,
ndipo Ine mwini ndidzakulangani mochulukitsa kasanu ndi kawiri chifukwa cha kuchimwa kwanu. 29 Mudzadya ana anu aamuna ndiponso
mudzadya ana anu aakazi. 30 Ine ndidzawononga malo anu opembedzera
mafano a ku mapiri. Ndidzagwetsa maguwa anu ofukizira lubani, ndipo ndidzawunjika pamodzi mitembo ya mafano anu wopanda moyowo,

ndipo ndidzanyansidwa nanu. [31] Ndidzasandutsa mizinda yanu kukhala
mabwinja ndi kuwononga malo anu wopatulika. Sindidzakondweranso
ndi fungo lokoma la zopereka zanu. [32] Ndidzawononga dziko kotero
kuti adani anu m'menemo adzadabwa. [33] Ndidzakubalalitsani pakati pa
mitundu ina ya anthu ndipo ndidzasolola lupanga langa ndi kukupirik-
itsani. Dziko lanu lidzawonongedwa, ndipo mizinda yanu idzasanduka
mabwinja. [34] Nthawi imeneyo nthaka idzasangalalira kuyipumitsa kwake
nthawi yonse imene idzakhala yosalimidwa, pamene inu mudzakhala
muli m'dziko la adani anu. Pa nthawi imeneyo dziko lidzapumula ndi
kukondwerera kulipumuza kwake. [35] Nthawi zonse pamene dzikolo lidza-
khala lopanda anthu, nthaka idzapumula. Mpumulo umenewu udzakhala
umene nthakayo sinapumulepo pa nthawi zimene inu munkapumula muli
m'dzikomo.

[36] " 'Kunena za amene adzatsale, ndidzayika mantha m'mitima mwawo
m'dziko la adani awo kotero kuti adzathawa ngakhale mtswatswa wa
tsamba lowuluka ndi mphepo. Adzathawa ngati akuthawa lupanga, ndipo
adzagwa pansi ngakhale padzakhale wopanda kuwapirikitsa. [37] Iwo adza-
phunthwitsana ngati akuthawa nkhondo, ngakhale padzakhale popanda
wowapirikitsa. Choncho simudzatha kuyima pamaso pa adani anu.
[38] Mudzatheratu pakati pa mitundu ya anthu. Dziko la adani anu
lidzakudyani. [39] Ngakhale iwo amene adzatsale adzatheratu m'dziko la
adani awo chifukwa cha machimo awo ndi machimo a makolo awo.

[40] " 'Tsono adzawulula machimo awo ndi machimo a makolo awo,
kusakhulupirika kwawo ndi mayendedwe awo otsutsana nane, [41] zomwe
zinandipangitsa kuwafulatira ndi kuwapereka m'manja mwa adani awo.
Ndipo mitima yawo yowumayo ikadzadzichepetsa ndi kuvomera ku-
langidwa chifukwa cha machimo awo, [42] Ine ndidzakumbukira pangano
langa ndi Yakobo, pangano langa ndi Isake, pangano langa ndi Abrahamu.
Ndidzakumbukiranso dzikolo. [43] Pakuti adzasiya dziko lawo lopanda
anthu, nthaka idzakondwerera zaka zake zoyipumuza pamene iwo kudza-
khala kulibe. Koma adzalangidwa chifukwa cha machimo awo popeza
anakana malamulo anga ndipo mitima yawo inkayipidwa nawo malangizo
anga. [44] Komabe ngakhale adzachite zonsezi ali m'dziko la adani awo,
Ine sindidzawakana kapena kuyipidwa nawo kwakuti n'kuwawononga
kwathunthu ndi kuthetsa pangano langa ndi iwo. Ine ndine Yehova Mu-
lungu wawo. [45] Koma powachitira chifundo, ndidzakumbukira pangano
langa ndi makolo awo amene ndinawatulutsa m'dziko la Igupto mitundu
ina ikuona kuti Ine ndikhale Mulungu wawo. Ine ndine Yehova.' "

[46] Amenewa ndi malamulo ndi malangizo amene Yehova anawayika
pakati pa Iye mwini ndi Aisraeli pa Phiri la Sinai kudzera mwa Mose.

# 27

### *Kuwombola Zomwe ndi za Yehova*

[1] Yehova anawuza Mose kuti, [2] "Yankhula ndi Aisraeli ndipo uwawuze
kuti, 'Ngati munthu anachita lumbiro lapadera loti adzapereka munthu
mnzake kwa Yehova ndipo akufuna kuti amuwombole, [3] mtengo wake
ukhale masekeli a siliva makumi asanu, molingana ndi kawerengedwe
ka ku Nyumba ya Mulungu, ngati munthuyo ndi wamwamuna wa zaka
zapakati pa 20 ndi 60. [4] Ndipo ngati ndi wamkazi, mtengo wake ukhale
masekeli makumi atatu. [5] Mtengo wa munthu wamwamuna wa zaka
zapakati pa zisanu ndi makumi awiri ukhale masekeli makumi awiri

ndipo munthu wamkazi ukhale masekeli khumi. 6 Ngati ndi munthu
wamwamuna wa pakati pa mwezi umodzi ndi zaka zisanu, mtengo wa
munthu wamwamuna ukhale masekeli asanu a siliva ndipo ngati ndi
wamkazi, ukhale masekeli atatu a siliva. 7 Ngati ndi munthu wa zaka
makumi asanu ndi limodzi kapena kuposerapo, mtengo wa wamwamuna
ukhale masekeli khumi ndi asanu, ndipo wamkazi ukhale masekeli khumi.
8 Ngati munthu amene anachita lumbiro ndi wosauka kwambiri kuti
sangathe kulipira ndalama zimenezo, abwere ndi munthu woperekedwa
uja kwa wansembe, ndipo wansembeyo ayike mtengo woti munthu
wolumbirayo angathe kulipira.

9 " 'Ngati chimene anachitira lumbiro kuti apereke ndi nyama imene
amapereka kukhala nsembe kwa Yehova, zonse zimene amapereka kwa
Yehova n'zopatulika. 10 Munthu asasinthanitse ndi ina kapena kupereka
ina yabwino m'malo mwa yoyipa, kapena yoyipa m'malo mwa yabwino.
Ngati asinthitsa nyama ina m'malo mwa ina, nyamayo pamodzi ndi inzake
wasinthitsayo zikhala zopatulika. 11 Ngati chimene anachitira lumbiro ndi
nyama yodetsedwa, nyama imene siloledwa kuyipereka kukhala nsembe
kwa Yehova, nyamayo abwere nayo kwa wansembe, 12 ndipo wansembeyo
atchule mtengo wake poona ngati ndi yabwino kapena ndi yoyipa. Mtengo
umene wansembe atchule ndiwo udzakhale mtengo wake. 13 Ngati mwini
wakeyo akufuna kuwombola nyamayo, awonjezere pa mtengo wake wa
nyamayo chimodzi mwa zigawo zisanu zamtengowo.

14 " 'Ngati munthu apereka nyumba yake kuti ikhale yopatulika kwa
Yehova, wansembe atchule mtengo wake poona ngati ndi yabwino kapena
ndi yoyipa. Mtengo umene wansembe atchule ndiwo udzakhale mtengo
wake. 15 Ngati munthu amene wapereka nyumbayo afuna kuyiwombola
nyumbayo, awonjezere pamtengo wake wa nyumbayo, limodzi mwa
magawo asanu amtengowo. Ndipo nyumbayo idzakhalanso yake.

16 " 'Ngati munthu apereka kwa Yehova mbali ina ya malo a makolo ake,
mtengo umene awuyike ukhale wolingana ndi mtengo wa mbewu zimene
zimadzabzalidwamo. Zikhale mbewu za barele za makilogalamu makumi
awiri ndipo mtengo wake ukhale masekeli makumi asanu. 17 Ngati
munthu apereka munda wake kuyambira chaka chokondwerera zaka
makumi asanu, mtengo wake ukhale umene unakhazikitsidwa. 18 Koma
ngati apereka mundawo chaka chokondwerera zaka makumi asanu chi-
tapita, wansembe adzatchula mtengo molingana ndi zaka zomwe zatsala
kuti chifike chaka china chokondwerera zaka makumi asanu, ndipo
mtengo wake udzakhala wotsikirapo. 19 Ngati munthu amene wapereka
munda afuna kuwuwombola, ayenera kuwonjezera pa mtengo wake wa
mundawo, limodzi mwa magawo asanu a mtengowo. Ndipo mundawo
udzakhalanso wake. 20 Koma ngati sawuwombola mundawo, kapena ngati
waugulitsa kwa munthu wina, mundawo sudzawomboledwanso. 21 Mwini
mundawo akawusiya m'chaka chokondwerera zaka makumi asanu ndiye
kuti mundawo udzakhala wopatulika monga woperekedwa kwa Yehova:
udzakhala munda wa ansembe.

22 " 'Ngati munthu apereka kwa Yehova munda umene anagula, umene
si malo a makolo ake, 23 wansembe atchule mtengo wake kufikira pa
chaka chokondwerera zaka makumi asanu, ndipo munthuyo apereke
ndalama zokwanira mtengo wake pa tsikulo monga ndalama zopatulika
kwa Yehova. 24 Pa chaka chokondwerera zaka makumi asanu, mundawo
udzabwezedwa kwa munthu amene anawugulitsayo, amene malowo anali
ake. 25 Potchula mtengo uliwonse wansembe awerengere molingana ndi

mtengo wa sekeli wa ku Nyumba ya Mulungu: magera makumi awiri pa
sekeli imodzi.
26 “ ‘Koma pasapezeke munthu wopereka mwana woyamba kubadwa
wa nyama, popeza mwana woyamba kubadwa ali kale wa Yehova, kaya
ndi ng’ombe kapena nkhosa, zimenezi ndi za Yehova. 27 Ngati ili nyama
yodetsedwa, ayiwombole pa mtengo umene wansembe wawuyika, ndi
kuwonjezeranso pa mtengo wake wa nyamayo, limodzi mwa magawo
asanu amtengowo. Ngati sayiwombola, igulitsidwe pa mtengo umene
wansembe awuyike.
28 “ ‘Koma chinthu chilichonse choperekedwa kwa Yehova, kaya ndi
munthu, nyama, kaya ndi malo a makolo, chimenechi chisagulit-
sidwe kapena kuwomboledwa. Choperekedwa kwa Yehova motere
n’chopatulika kwambiri.
29 “ ‘Munthu amene waperekedwa kotheratu sangawomboledwe.
Munthuyo ayenera kuphedwa.
30 “ ‘Chakhumi chilichonse chochokera m’dziko, kaya ndi tirigu wochok-
era m’nthaka kapena chipatso cha m’mitengo ndi za Yehova. Chimene-
cho ndi chopatulika kwa Yehova. 31 Ngati munthu afuna kuwombola
chakhumi chilichonse, awonjezere pamtengo wake chimodzi mwa zigawo
zisanu za mtengowo. 32 Chakhumi cha ng’ombe ndi nkhosa, kapena
kuti nyama iliyonse ya khumi imene m’busa wayiwerenga idzakhala
yopatulikira kwa Yehova. 33 Palibe amene adzaloledwa kusankha nyama
yomwe ili yabwino kapena kusinthitsa. Ngati asinthitsa, nyamayo
pamodzi ndi inzakeyo zidzakhala zopatulika ndipo sangaziwombole.’ ”
34 Amenewa ndi malamulo amene Yehova anamupatsa Mose pa Phiri la
Sinai kuti awuze Aisraeli.

# Numeri

*Kalembera*

1 Yehova anayankhula ndi Mose m'chipululu cha Sinai, mu tenti ya
msonkhano, pa tsiku loyamba la mwezi wachiwiri, m'chaka chachiwiri
atatuluka mu Igupto, kuti, 2 "Werengani Aisraeli onse m'mafuko awo
ndi m'mabanja awo, lemba dzina la munthu wamwamuna aliyense,
mmodzimmodzi. 3 Iwe ndi Aaroni mwawerenge mwa magulu awo mu
Israeli, amuna onse a zaka makumi awiri zakubadwa ndi opitirirapo
omwe angathe kugwira ntchito ya usilikali. 4 Munthu mmodzi wochokera
ku fuko lililonse yemwe ndi mtsogoleri wa banja lake, ndiye akuthandizeni
pa ntchitoyi. 5 Mayina a anthu amene akuthandizeniwo ndi awa:

Elizuri mwana wa Sedeuri, kuchokera ku fuko la Rubeni,
6 Selumieli mwana wa Zurisadai, kuchokera ku fuko la Simeoni,
7 Naasoni mwana wa Aminadabu, kuchokera ku fuko la Yuda,
8 Netanieli mwana wa Zuwara, kuchokera ku fuko la Isakara,
9 Eliabu mwana wa Heloni, kuchokera ku fuko la Zebuloni,
10 Mwa ana a Yosefe:
kuchokera ku fuko la Efereimu, Elisama mwana wa Amihudi;
kuchokera ku fuko la Manase, Gamalieli mwana wa Pedazuri;
11 Abidani mwana wa Gideoni, kuchokera ku fuko la Benjamini,
12 Ahiyezeri mwana wa Amisadai, kuchokera ku fuko la Dani,
13 Pagieli mwana wa Okirani, kuchokera ku fuko la Aseri,
14 Eliyasafu mwana wa Deuweli, kuchokera ku fuko la Gadi,
15 Ahira mwana wa Enani, kuchokera ku fuko la Nafutali."

16 Amenewa ndi anthu amene anasankhidwa kuchokera m'magulu
mwawo, eni mbumba a mafuko a makolo awo. Iwowa anali atsogoleri
a mafuko a Israeli.
17 Mose ndi Aaroni anatenga anthu amene mayina awo anaperekedwa,
18 ndipo pa tsiku loyamba la mwezi wachiwiri, anasonkhanitsa anthu
onse pamodzi. Anthuwo anafotokoza za makolo awo mwa mafuko
awo ndi mabanja awo. Ndipo mayina a amuna onse amene anali ndi
zaka makumi awiri kapena kupitirirapo analembedwa, mmodzimmodzi
19 monga momwe Yehova analamulira Mose. Motero iyeyo anawawerenga
m'chipululu cha Sinai:

20 Kuchokera mwa ana a Rubeni, mwana wamwamuna woyamba wa Israeli:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali, anawalemba mayina awo,
mmodzimmodzi monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja
awo. 21 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Rubeni chinali
46,500.

22 Kuchokera mwa zidzukulu za Simeoni:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina awo,

mmodzimmodzi monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja
awo. 23 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Simeoni chinali
59,300.

24 Kuchokera mwa zidzukulu za Gadi:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
25 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Gadi chinali 45, 650.

26 Kuchokera mwa zidzukulu za Yuda:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
27 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Yuda chinali 74, 600.

28 Kuchokera mwa zidzukulu za Isakara:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
29 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Isakara chinali
54,400.

30 Kuchokera mwa zidzukulu za Zebuloni:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
31 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Zebuloni chinali
57,400.

32 Kuchokera mwa ana aamuna a Yosefe:
Kuchokera mwa zidzukulu za Efereimu:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
33 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Efereimu chinali
40,500.

34 Kuchokera mwa zidzukulu za Manase:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
35 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Manase chinali
32,200.

36 Kuchokera mwa zidzukulu za Benjamini:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
37 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Benjamini chinali
35,400.

38 Kuchokera mwa zidzukulu za Dani:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
39 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Dani chinali 62,700.

40 Kuchokera mwa zidzukulu za Aseri:
Amuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
41 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Aseri chinali 41,500.

42 Kuchokera mwa zidzukulu za Nafutali:
Aamuna onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo, omwe
akanatha kugwira ntchito ya usilikali anawalemba mayina
awo monga mwa mbiri ya mafuko awo ndi mabanja awo.
43 Chiwerengero cha anthu ochokera m'fuko la Nafutali chinali
53,400.

44 Amenewa ndiwo anthu amene Mose ndi Aaroni anawawerenga
mothandizidwa ndi atsogoleri khumi ndi awiri a Israeli, aliyense kuyimira
fuko lake. 45 Aisraeli onse a zaka makumi awiri kapena kupitirirapo,
omwe akanatha kugwira ntchito ya usilikali m'gulu lankhondo la Israeli
anawawerenga monga mwa mabanja awo. 46 Chiwerengero cha anthu
onse pamodzi chinali 603,550.

47 Koma mabanja a fuko la Levi okha sanawawerenge pamodzi ndi
ena. 48 Pakuti Yehova anawuza Mose kuti, 49 "Usawerenge fuko la
Levi kapena kuliphatikiza m'kawundula wa Aisraeli. 50 Koma uyike
Aleviwo kuti aziyang'anira tenti yanga yopatulika, zipangizo zake ndi
zonse zili m'menemo. Azinyamula tentiyo pamodzi ndi zipangizo zake
zonse; azisamalira ndi kumanga misasa mozungulira tentiyo. 51 Pamene
akusamutsa tentiyo, Alevi ndiwo aziyitsitsa, akafuna kuyimanganso, Alevi
ndiwo aziyimiritsa. Wina aliyense amene adzayandikire tentiyo adza-
phedwa. 52 Aisraeli azimanga matenti awo m'magulumagulu, munthu
aliyense ku gulu lake pansi pa mbendera yake. 53 Alevi nawonso, azimanga
matenti awo mozungulira tenti yopatulika kuti chilango chisagwere Ais-
raeli onse. Ndipo Alevi aziyang'anira ndi kusamalira tenti yopatulikayo."

54 Choncho Aisraeli anachita monga Yehova analamulira Mose.

# 2

*Malo a Misasa ya Mafuko Onse a Aisraeli*

1 Yehova anati kwa Mose ndi Aaroni: 2 "Aisraeli azimanga misasa yawo
mozungulira tenti ya msonkhano motalikira pang'ono. Munthu aliyense
amange pamene pali mbendera ya fuko lake."

3 Kummawa, kotulukira dzuwa, magulu a msasa wa Yuda amange
pamene pali mbendera yawo. Mtsogoleri wa Ayudawo ndi Naasoni
mwana wa Aminadabu. 4 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo ndi
74,600.

5 Fuko la Isakara lidzamanga pafupi ndi Yuda. Mtsogoleri wa gulu la
Isakara ndi Netanieli mwana wa Zuwara. 6 Chiwerengero cha gulu lake
lankhondo ndi 54,400.
7 Lotsatira lidzakhala fuko la Zebuloni. Mtsogoleri wa gulu la Zebuloni
ndi Eliabu mwana wa Heloni. 8 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo
ndi 57,400.
9 Anthu onse aamuna m'misasa ya Yuda, chiwerengero chawo ndi
186,400 monga mwa magulu awo. Iwowo ndiwo aziyamba kusamuka.

10 Kummwera kudzakhala magulu a msasa wa Rubeni pamene pali
mbendera yawo. Mtsogoleri wa gulu la Rubeni ndi Elizuri mwana wa
Sedeuri. 11 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo ndi 46,500.
12 Fuko la Simeoni lidzamanga pafupi ndi Rubeni. Mtsogoleri wa gulu
la Simeoni ndi Selumieli mwana wa Zurisadai. 13 Chiwerengero cha gulu
lake lankhondo ndi 59,300.
14 Lotsatira lidzakhala fuko la Gadi. Mtsogoleri wa gulu la Gadi ndi
Eliyasafu mwana wa Deuweli. 15 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo
ndi 45,650.
16 Anthu onse aamuna mu msasa wa Rubeni, chiwerengero chawo
monga mwa magulu awo, ndi 151,450. Iwowo azikhala achiwiri
posamuka.

17 Tsono tenti ya msonkhano ndi msasa wa Alevi zidzakhala pakati pa
misasayo. Iwo adzasamuka monga momwe anamangira misasa yawo,
aliyense pa malo ake pamene pali mbendera yake.

18 Kumadzulo kudzakhala magulu a msasa wa Efereimu pamene pali
mbendera yawo. Mtsogoleri wa Aefereimuwo ndi Elisama mwana wa
Amihudi. 19 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo ndi 40,500.
20 Fuko la Manase lidzakhala pafupi ndi Efereimu. Mtsogoleri wa
Amanase ndi Gamalieli mwana wa Pedazuri. 21 Chiwerengero cha gulu
lake lankhondo ndi 32,200.
22 Lotsatira lidzakhala fuko la Benjamini. Mtsogoleri wa Abenjamini
ndi Abidani mwana wa Gideoni. 23 Chiwerengero cha gulu lake
lankhondo ndi 35,400.
24 Anthu onse aamuna mu msasa wa Efereimu, chiwerengero chawo
ndi 108,100 monga mwa magulu awo. Iwowo azikhala achitatu
posamuka.

25 Kumpoto kudzakhala msasa wa magulu a Dani pamene pali
mbendera yawo. Mtsogoleri wa Adani ndi Ahiyezeri mwana wa
Amisadai. 26 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo ndi 62,700.
27 Fuko la Aseri lidzamanga pafupi ndi iwowo. Mtsogoleri wa Aaseri
ndi Pagieli mwana wa Okirani. 28 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo
ndi 41,500.
29 Lotsatira lidzakhala fuko la Nafutali. Mtsogoleri wa Anafutali ndi
Ahira mwana wa Enani. 30 Chiwerengero cha gulu lake lankhondo ndi
53,400.
31 Anthu onse aamuna mu msasa wa Dani chiwerengero chawo ndi
157,600. Iwo azidzanyamuka pomaliza, ndi mbendera zawo.

32 Amenewa ndi Aisraeli monga mwa mabanja a makolo awo.

Chiwerengero cha Aisraeli onse m'misasa chinali 603,550, mwa magulu
awo. 33 Koma Alevi sanawawerenge pamodzi ndi Aisraeli enawo monga
momwe Yehova analamulira Mose.

34 Choncho Aisraeli anachita zonse zomwe Yehova analamulira Mose.
Umo ndi momwe amamangira misasa yawo pamene panali mbendera
zawo, ndipo ankasamuka monga mwa mafuko a makolo awo.

# 3

*Alevi*

1 Iyi ndi mbiri ya banja la Aaroni ndi Mose pa nthawi yomwe Yehova
anayankhula ndi Mose pa phiri la Sinai.

2 Mayina a ana aamuna a Aaroni anali Nadabu, woyamba kubadwa,
Abihu, Eliezara ndi Itamara. 3 Amenewa ndi mayina a ana aamuna a
Aaroni, ansembe odzozedwa omwe anapatulidwa kuti azitumikira ngati
ansembe. 4 Koma Nadabu ndi Abihu, anagwa nafa pamaso pa Yehova
pamene ankapereka nsembe ndi moto wachilendo pamaso pa Yehova
m'chipululu cha Sinai. Iwowo analibe ana aamuna. Choncho Eliezara ndi
Itamara ndiwo amene ankatumikira ngati ansembe nthawi imene Aaroni
abambo awo anali moyo.

5 Yehova anati kwa Mose, 6 "Bweretsa fuko la Levi ndipo ulipereke
kwa Aaroni wansembe kuti lizimutumikira. 7 Azigwira ntchito yothandiza
iyeyo ndi gulu lonse ku tenti ya msonkhano pogwira ntchito ya ku
Chihema. 8 Azisamalira zipangizo zonse za mu tenti ya msonkhano,
ndipo azigwirira ntchito Aisraeli potumikira mu tenti. 9 Pereka Alevi
kwa Aaroni ndi kwa ana ake aamuna. Amenewa ndiwo Aisraeli amene
aperekedwa kwa iye kwathunthu. 10 Usankhe Aaroni ndi ana ake aamuna
kuti azitumikira pa ntchito ya unsembe. Koma wina aliyense woyandikira
malo opatulika aphedwe."

11 Yehova anawuzanso Mose kuti, 12 "Pakati pa Aisraeli onse ndatenga
Alevi kulowa m'malo mwa mwana wamwamuna aliyense woyamba
kubadwa kwa amayi a Chiisraeli. Alevi ndi anga, 13 pakuti ana onse
oyamba kubadwa ndi anga. Nditakantha ana onse oyamba kubadwa mu
Igupto, ndinadzipatulira ndekha mwana aliyense woyamba kubadwa mu
Israeli, wa munthu ndi nyama. Azikhala anga. Ine ndine Yehova."

14 Yehova anawuza Mose m'chipululu cha Sinai kuti, 15 "Werenga Alevi
monga mwa mabanja awo ndi mafuko awo. Werenga mwamuna aliyense
kuyambira wa mwezi umodzi kapena kupitirirapo." 16 Choncho Mose
anawawerenga potsatira zomwe Yehova anamulamulira.

17 Mayina a ana aamuna a Levi ndi awa:
Geresoni, Kohati ndi Merari.
18 Mayina a ana a Geresoni potsata mabanja awo ndi awa:
Libini ndi Simei.
19 Ana a Kohati potsata mabanja awo ndi awa:
Amramu, Izihari, Hebroni ndi Uzieli.
20 Ana a Merari potsata mabanja awo ndi awa:
Mali ndi Musi.

Amenewa ndiwo anali mabanja a Alevi monga mwa makolo awo.

21 Kwa Geresoni kunali banja la Alibini, banja la Asimei. Amenewa
ndiwo anali mabanja a Ageresoni. 22 Chiwerengero cha amuna onse
amene anawawerenga a mwezi umodzi kapena kupitirirapo chinali 7,500.
23 Mabanja a Ageresoni azimanga misasa yawo kumadzulo, kumbuyo kwa
Chihema. 24 Mtsogoleri wa mabanja a Ageresoni anali Eliyasafu mwana
wa Laeli. 25 Ntchito imene Ageresoni anapatsidwa ku tenti ya msonkhano
inali yosamalira Chihema ndi tenti, pamodzi ndi zophimbira zake, katani
ya pa khomo la ku tenti ya msonkhano, 26 ndi makatani wotchinga bwalo,
katani ya pa chipata cholowera ku bwalo lozungulira Chihema ndi guwa
lansembe, zingwe ndi zonse zokhudzana ndi ntchito yawo.

27 Kwa Kohati kunali mabanja a Amramu, Aizihara, Ahebroni ndi
Auzieli. Awa ndiye anali mabanja a Akohati. 28 Chiwerengero cha
amuna onse a mwezi umodzi kapena kupitirirapo chinali 8,600. Akohati
ankagwira ntchito yosamalira malo wopatulika. 29 Mabanja a ana a Kohati
ankamanga misasa yawo kummwera kwa Chihema. 30 Mtsogoleri wa
magulu a mabanja a Kohati anali Elizafani mwana wa Uzieli. 31 Iwo ank-
agwira ntchito yosamalira Bokosi la Chipangano, tebulo, choyikapo nyale,
maguwa, zipangizo za kumalo wopatulika zimene ansembe ankagwiritsa
ntchito, katani, ndi zonse zomwe ankagwiritsa ntchito. 32 Mtsogoleri
wamkulu wa Alevi anali Eliezara mwana wa Aaroni wansembe. Iye
anasankhidwa kukhala woyang'anira omwe ankasamalira malo wopat-
ulika.

33 Kwa Merari kunali banja la Mali ndi banja la Musi. Amenewa ndiye
anali mabanja a Amerari. 34 Chiwerengero cha amuna onse kuyambira a
mwezi umodzi kapena kupitirirapo chinali 6,200. 35 Mtsogoleri wa magulu
a mabanja a Amerari anali Zuriyeli mwana wa Abihaili. Iwo ankamanga
misasa yawo kumpoto kwa Chihema. 36 Amerari anapatsidwa ntchito
yosamalira mitengo ya chihema, nsichi zake, mizati yake, matsinde ake,
ndi zida zake zonse, ndi zonse zomwe ankagwiritsa ntchito, 37 pamodzi
ndi mizati yozungulira bwalo ndi matsinde ake, zikhomo za chihema ndi
zingwe zake.

38 Mose ndi Aaroni ndi ana ake aamuna ankamanga misasa yawo
kummawa kwa chihema, kuyang'ana kotulukira dzuwa, kutsogolo kwa
tenti ya msonkhano. Anali ndi ntchito yosamalira malo wopatulika
m'malo mwa Aisraeli. Aliyense woyandikira malo wopatulika ankayenera
kuphedwa.

39 Alevi onse amene Mose ndi Aaroni anawawerenga potsatira lamulo
la Yehova monga mwa magulu a mabanja awo, amuna onse kuyambira a
mwezi umodzi kapena kupitirirapo anali 22,000.

40 Yehova anawuza Mose kuti, "Werenga ana onse aamuna oyamba
kubadwa mu Israeli, omwe ali ndi mwezi umodzi kapena kupitirirapo
ndipo ulembe mndandanda wa mayina awo. 41 Unditengere Alevi
onse m'malo mwa ana oyamba kubadwa onse a Aisraeli, ndiponso
ziweto zazimuna za Alevi m'malo mwa ziweto zonse zazimuna zoyamba
kubadwa za Aisraeli. Ine ndine Yehova."
42 Choncho Mose anawerenga ana aamuna onse oyamba kubadwa a
Aisraeli monga momwe Yehova anamulamulira. 43 Chiwerengero chonse

cha ana aamuna oyamba kubadwa kuyambira a mwezi umodzi kapena
kupitirirapo chinali 22, 273.
44 Ndipo Yehova anawuzanso Mose kuti, 45 “Tenga Alevi m’malo mwa
ana aamuna oyamba kubadwa onse a Aisraeli, ndiponso zoweta zonse za
Alevi m’malo mwa zoweta za Aisraeli. Alevi ndi anga. Ine ndine Yehova.
46 Pofuna kuwombola ana aamuna 273 oyamba kubadwa a Aisraeli amene
anaposa chiwerengero cha aamuna a fuko la Levi, 47 utenge masekeli
asanu pa munthu aliyense. Masekeliwo akhale ofanana ndi masekeli a
ku malo wopatulika, kumene sekeli imodzi imakwanira magera makumi
awiri. 48 Ndalama zimenezi uzipereke kwa Aaroni ndi ana ake aamuna
kuti ukhale mtengo woombolera Aisraeli woonjezerawo.”
49 Choncho Mose anatenga ndalama zowombolera zija kuchokera kwa
Aisraeli amene chiwerengero chawo chinaposa chiwerengero cha omwe
anawomboledwa ndi Alevi. 50 Anatenga masekeli a siliva okwana 1,365
molingana ndi masekeli a ku malo opatulika, kuchokera kwa ana aamuna
oyamba kubadwa a Aisraeli. 51 Mose anapereka ndalama zowombolera
zija kwa Aaroni ndi ana ake aamuna monga mwa mawu amene Yehova
analamulira.

# 4

*Akohati*

1 Yehova anati kwa Mose ndi Aaroni: 2 “Werengani Akohati omwe
ndi gawo limodzi la Alevi monga mwa mafuko awo ndi mabanja awo.
3 Werengani amuna onse amene ali ndi zaka makumi atatu mpaka
zaka makumi asanu amene amabwera kudzagwira ntchito mu tenti ya
msonkhano.
4 “Ntchito ya Akohati mu tenti ya msonkhano ndi iyi: kusamalira zinthu
zopatulika kwambiri. 5 Pamene anthu akusamuka pa msasa, Aaroni ndi
ana ake aamuna azilowa mu tenti ndi kuchotsa chinsalu chotchingira ndi
kuphimba nacho bokosi la umboni. 6 Ndipo azikuta bokosilo ndi zikopa za
akatumbu ndi kuyala pamwamba pake nsalu ya mtundu wa thambo ndi
kuyika mitengo yonyamulira m’malo mwake.
7 “Pa tebulo pamene pamakhala buledi wa ansembe aziyalapo nsalu
ya mtundu wa thambo, ndipo aziyikapo mbale, mabeseni, zipande
ndi mitsuko yoperekera nsembe yachakumwa. Aziyikaponso buledi
wokhala pamenepo nthawi zonse. 8 Tsono pamwamba pa izi aziyalapo
nsalu yofiira, ndi kuzikuta m’zikopa za akatumbu ndi kuyika mitengo
yonyamulira m’malo mwake.
9 “Azitenga nsalu ya mtundu wa thambo ndi kukutira choyikapo nyale,
pamodzi ndi nyale zake, zopanira zake, zotengera zake ndi mitsuko yonse
yosungiramo mafuta. 10 Kenaka achikulunge pamodzi ndi zipangizo zake
zonse m’zikopa za akatumbu ndi kuchiyika pa chonyamulira chake.
11 “Pamwamba pa guwa la golide aziyalapo nsalu ya mtundu wa thambo
ndi kukutira ndi zikopa za akatumbu ndi kuyika m’malo mwake mitengo
yonyamulira.
12 “Azitenga zipangizo zonse zogwiritsira ntchito ku malo wopatulika,
azizikulunga m’nsalu ya mtundu wa thambo, azizikuta ndi zikopa za
akatumbu ndi kuziyika pa zonyamulira zake.
13 “Azichotsa phulusa la pa guwa lansembe lamkuwa ndi kuyalapo
nsalu yapepo pamwamba pake. 14 Kenaka aziyikapo zipangizo zonse zog-
wiritsira ntchito potumikira pa guwa, kuphatikizapo miphika yowotchera

nyama, mafoloko otengera nyama, zowolera phulusa ndi mbale zowazira
magazi pa guwa lansembe ndipo pamwamba pake aziyalapo zikopa za
akatumbu ndi kuziyika m'zonyamulira zake.
15 "Aaroni ndi ana ake aamuna akamaliza kukutira ziwiya za ku
malo wopatulika ndi zipangizo zopatulika zonse, ndipo akakonzeka
kusamuka pamalopo, Akohati abwere kudzazinyamula koma asagwire
zinthu zopatulikazo. Akatero adzafa. Izi ndizo zinthu zimene Akohati
ayenera kunyamula mu tenti ya msonkhano.
16 "Eliezara mwana wa Aaroni, wansembe, aziyang'anira mafuta a
nyale, ndi lubani wa nsembe zofukiza, nsembe yaufa yoperekedwa nthawi
zonse ndi mafuta odzozera. Aziyang'aniranso chihema ndi zonse zili
m'menemo, kuphatikizapo zida ndi ziwiya zonse zopatulika."
17 Yehova anawuzanso Mose ndi Aaroni kuti, 18 "Onetsetsani kuti
mabanja a fuko la Kohati asachotsedwe kwa Alevi. 19 Koma muziwachitira
izi kuti asafe, akhalebe ndi moyo pamene ayandikira zinthu za ku malo
wopatulika kwambiri: Aaroni ndi ana ake aamuna azipita ku malo
wopatulika ndi kumamupatsa munthu aliyense ntchito yake ndi zimene
ayenera kunyamula. 20 Koma Akohati asalowe kukaona zinthu zopatulika,
ngakhale kanthawi pang'ono, chifukwa akatero adzafa."

### *Ageresoni*

21 Yehova anawuza Mose kuti, 22 "Werenganso Ageresoni monga mwa
mabanja ndi mafuko awo. 23 Uwerenge amuna onse a zaka makumi
atatu mpaka a zaka makumi asanu zakubadwa amene amabwera kudza-
tumikira ku tenti ya msonkhano.
24 "Ntchito ya mafuko a Ageresoni pamene akugwira ntchito ndi
kunyamula katundu ndi iyi: 25 Azinyamula makatani a ku chihema, tenti
ya msonkhano, zokutira zake ndi zokutira kunja za zikopa za akatumbu,
makatani a pa khomo la ku tenti ya msonkhano, 26 makatani wotchingira
bwalo lozungulira chihema ndi guwa, katani ya pa khomo, zingwe ndi zida
zonse zimene zimagwiritsidwa ntchito m'chihema. Ageresoni azichita
zonse zofunika kuchitika ndi zinthu zimenezi. 27 Ntchito yawo yonse, kaya
kunyamula kapena kugwira ntchito zina, achite Ageresoni motsogozedwa
ndi Aaroni ndi ana ake aamuna. Uwagawire ntchito zonse zimene
akuyenera kugwira. 28 Iyi ndiye ntchito ya fuko la Ageresoni ku tenti ya
msonkhano. Ntchito zawo zichitike motsogozedwa ndi Itamara mwana
wa wansembe Aaroni.

### *Amerari*

29 "Werenga Amerari monga mwa mafuko awo ndi mabanja awo.
30 Werenga amuna onse a zaka makumi atatu mpaka zaka makumi
asanu zakubadwa amene akatumikire mu tenti ya msonkhano. 31 Ntchito
yawo pamene azikatumikira mu tenti ya msonkhano ndi iyi: kunyamula
matabwa a chihema, mitanda, mizati ndi matsinde, 32 ndiponso mizati
yozungulira bwalo ndi matsinde ake, zikhomo za chihema, zingwe ndi
zipangizo zake zonse ndiponso zonse zokhudzana ndi ntchito yake. Uwuze
munthu aliyense chomwe ayenera kuchita. 33 Iyi ndiyo ntchito ya
mafuko a Amerari pamene akugwira ntchito ku tenti ya msonkhano
motsogozedwa ndi Itamara mwana wa wansembe Aaroni."

### *Chiwerengero cha Fuko la Levi*

34 Mose, Aaroni ndi atsogoleri a magulu a anthu anawerenga Akohati
monga mwa mafuko ndi mabanja awo. 35 Aamuna onse a zaka makumi

atatu mpaka makumi asanu amene anabwera kudzagwira ntchito ku tenti
ya msonkhano, [36] atawawerenga mwa mafuko awo, anali 2,750. [37] Ichi
chinali chiwerengero cha mafuko a Akohati onse omwe ankatumikira mu
tenti ya msonkhano. Mose ndi Aaroni anawawerenga monga mwa lamulo
la Yehova.
[38] Ageresoni anawerengedwanso monga mwa mafuko ndi mabanja
awo. [39] Amuna onse a zaka makumi atatu mpaka makumi asanu amene
anabwera kudzagwira ntchito ku tenti ya msonkhano, [40] atawawerenga
mwa mafuko ndi mabanja awo, anali 2,630. [41] Ichi chinali chiwerengero
cha Ageresoni mwa mabanja awo amene ankatumikira ku tenti ya
msonkhano. Mose ndi Aaroni anawawerenga monga mwa lamulo la
Yehova.
[42] Amerari anawawerenga monga mwa mafuko ndi mabanja awo.
[43] Amuna onse kuyambira zaka makumi atatu mpaka makumi asanu
amene anabwera kudzatumikira ntchito mu tenti ya msonkhano,
[44] atawawerenga mwa mafuko ndi mabanja awo, anali 3,200. [45] Ichi
ndicho chinali chiwerengero cha mabanja a Amerari. Mose ndi Aaroni
anawawerenga monga momwe Yehova anawalamulira kudzera mwa
Mose.
[46] Kotero Mose, Aaroni ndi atsogoleri a Israeli anawerenga Alevi onse
monga mwa mafuko ndi mabanja awo. [47] Aamuna onse a zaka makumi
atatu mpaka zaka makumi asanu omwe anabwera kudzagwira ntchito
yonyamula zinthu ku tenti ya msonkhano [48] analipo 8,580. [49] Aliyense
anamupatsa ntchito ndi kumuwuza choti anyamule monga mwa lamulo
la Yehova kudzera mwa Mose.
Anawawerenga chomwechi potsata zimene Yehova analamula Mose.

# 5

### *Ukhondo wa pa Msasa*

[1] Yehova anawuza Mose kuti, [2] “Lamula Aisraeli kuti achotse mu msasa
aliyense amene ali ndi matenda opatsirana a pa khungu kapena matenda
otuluka madzi m’thupi a mtundu uliwonse, kapena aliyense wodetsedwa
chifukwa cha munthu wakufa. [3] Muchotse amuna komanso amayi ndipo
muwatulutsire kunja kwa msasa kuti asadetse msasa wawo kumene Ine
ndimakhala pakati pawo.” [4] Aisraeli anachitadi zimenezi. Anawatulutsira
kunja kwa msasa monga momwe Yehova analamulira Mose.

### *Kukonza Zolakwika*

[5] Yehova anati kwa Mose, [6] “Uza Aisraeli kuti, ‘Pamene mwamuna
kapena mayi walakwira mnzake mwa njira iliyonse, ndiye kuti ndi
wosakhulupirika pamaso pa Yehova. Munthuyo ndi wochimwa ndithu
ndipo [7] ayenera kuwulula tchimo limene anachitalo. Ayenera kubweza
zonse zimene anawononga, ndipo awonjezerepo chimodzi mwa magawo
asanu ndi kuzipereka kwa munthu amene anamulakwirayo. [8] Ngati
wolakwiridwayo alibe m’bale komwe kungapite zinthu zobwezedwazo,
zinthuzo zikhale za Yehova ndipo azipereke kwa wansembe, pamodzi
ndi nkhosa yayimuna ya nsembe yopepesera tchimo lake. [9] Zopereka
zonse zopatulika zomwe Aisraeli abwera nazo kwa wansembe zikhale za
wansembeyo. [10] Mphatso zilizonse zopatulika ndi za munthuyo, koma
zomwe wapereka kwa wansembe ndi za wansembeyo.’ ”

### *Mkazi Wosakhulupirika*

11 Kenaka Yehova anawuza Mose kuti, 12 “Yankhula ndi Aisraeli ndipo
uwawuze kuti, ‘Ngati mkazi wa munthu wina ayenda njira yosayenera
nakhala wosakhulupirika kwa mwamuna wake, 13 nakagonana ndi
mwamuna wina koma mwamuna wake wosadziwa, ndipo palibe wina
aliyense wadziwa za kudzidetsa kwake (pakuti palibe mboni yomuneneza
chifukwa sanagwidwe akuchita), 14 mwamuna wake ndi kuyamba kuchita
nsanje ndi kukayikira mkazi wakeyo kuti ndi wodetsedwa, komanso ngati
amuchitira nsanje ndi kumukayikira ngakhale asanadzidetse, 15 apite
naye mkaziyo kwa wansembe. Ndipo popita atengenso gawo lakhumi la
chopereka chaufa wa barele wokwana kilogalamu imodzi m’malo mwa
mkaziyo. Asathire mafuta pa nsembeyo kapena lubani, chifukwa ndi
nsembe ya chopereka ya chakudya yopereka chifukwa cha nsanje, nsembe
yozindikiritsa tchimo.’ ”

16 “ ‘Wansembe abwere naye mkaziyo ndi kumuyimitsa pamaso pa
Yehova. 17 Ndipo wansembeyo atenge madzi oyera m’mbiya ya dothi ndi
kuyika m’madzimo fumbi lapansi la m’Tenti ya Msonkhano. 18 Wansembe
atayimika mkaziyo pamaso pa Yehova, amumasule tsitsi lake, ndipo
ayike m’manja mwake nsembe yozindikiritsa tchimo, nsembe yachakudya
ya nsanje, wansembeyo atanyamula madzi owawa omwe amabweretsa
temberero.’ 19 Kenaka wansembeyo alumbiritse mkaziyo ndi kuti, ‘Ngati
mwamuna wina aliyense sanagonane ndi iwe ndipo sunayende njira
yoyipa ndi kukhala wodetsedwa pomwe uli pa ukwati ndi mwamuna
wako, madzi owawa awa omwe amabweretsa temberero asakupweteke.
20 Koma ngati wayenda njira yoyipa uli pa ukwati ndi mwamuna wako
ndi kudzidetsa pogonana ndi mwamuna amene si mwamuna wako,’
21 pamenepo wansembe alumbiritse mkaziyo ndi mawu a matemberero
ndi kumuwuza kuti, ‘Yehova achititse anthu ako kukutemberera ndi
kukunyoza pamene awononga ntchafu yako ndi kutupitsa mimba yako.
22 Madzi awa obweretsa temberero alowe m’thupi mwako ndi kutupitsa
mimba yako ndi kuwononga ntchafu yako.’ ”

“Pamenepo mkaziyo anene kuti, ‘Ameni, ameni.’ ”

23 “ ‘Wansembe alembe matemberero amenewa m’buku ndi kuwanyika
m’madzi owawa aja. 24 Amwetse mkaziyo madzi owawawo omwe
amabweretsa temberero, ndipo madzi amenewo adzalowa m’mimba
mwake ndi kuyambitsa ululu woopsa. 25 Wansembe achotse m’manja
mwa mkaziyo nsembe yachakudya ya nsanje ija, nayiweyula pamaso
pa Yehova ndi kuyipereka pa guwa lansembe. 26 Tsono wansembeyo
atapeko ufa dzanja limodzi kuti ukhale wachikumbutso ndi kuwutentha
pa guwa lansembe. Atatha izi, amwetse mkaziyo madzi aja. 27 Ndipo
ngati mkaziyo anadzidetsadi ndi kukhala wosakhulupirika kwa mwa-
muna wake, pamene amwa madzi obweretsa matemberero aja, nalowa
m’mimba mwake, adzamva ululu woopsa. Mimba yake idzatupa ndi
ntchafu yake idzawonongeka ndipo adzakhala wotembereredwa pakati
pa anthu ake. 28 Koma ngati mkaziyo sanadzidetse ndi kuti alibe tchimo,
adzakhala wopanda mlandu ndipo adzabereka ana.

29 “ ‘Limeneli ndiye lamulo la nsanje pamene mkazi wayenda njira
yoyipa ndi kudzidetsa ali pa ukwati ndi mwamuna wake, 30 kapena
pamene maganizo a nsanje abwera kwa mwamuna wake chifukwa
chokayikira mkazi wakeyo. Wansembe azitenga mkazi wotere ndi
kumuyimiritsa pamaso pa Yehova ndipo agwiritse ntchito lamulo lonseli

kwa mkaziyo. [31] Mwamunayo adzakhala wopanda tchimo lililonse, koma
mkaziyo adzasenza zotsatira za tchimo lake.’ ”

# 6

*Za Mnaziri*

[1] Yehova anawuza Mose kuti, [2] “Yankhula ndi Aisraeli ndipo uwawuze
kuti, ‘Ngati mwamuna kapena mkazi afuna kuchita lonjezo lapadera,
lonjezo lodzipatula yekha kwa Yehova ngati Mnaziri, [3] sayenera kumwa
vinyo kapena zakumwa zosasa ndipo asamamwe chakumwa chilichonse
cha mphesa. Asamamwe madzi a mphesa kapena kudya mphesa zaziwisi
kapena zowuma. [4] Pa nthawi yonse imene ali Mnaziri, asamadye
chilichonse chopangidwa kuchokera ku mphesa ngakhale mbewu zake
kapena makungu ake.’

[5] “ ‘Pa nthawi yonse ya lonjezo lodzipatula yekhalo, asamete kumutu
kwake ndi lumo. Akhale wopatulika mpaka nthawi yake yonse ya
kudzipatula yekha kwa Yehova itatha. Alileke tsitsi la pamutu pake kuti
likule.’ [6] Pa nthawi yonse imene munthuyo wadzipatula yekha kwa
Yehova asayandikire mtembo. [7] Ngakhale abambo ake kapena amayi ake
kapena mchimwene wake kaya mchemwali wake atamwalira, asadzidetse
pokhudza mitembo yawo chifukwa kulumbira kwake kwa kudzipatula
yekha kwa Yehova kuli pamutu pake. [8] Munthuyo ndi wopatulika masiku
onse odzipereka kwake kwa Yehova.

[9] “Ngati munthu wina afa mwadzidzidzi pafupi naye ndi kudetsa
tsitsi lake loperekedwalo, amete mutu wake pa tsiku lodziyeretsa, tsiku
lachisanu ndi chiwiri. [10] Tsono pa tsiku lachisanu ndi chitatu abweretse
nkhunda ziwiri kapena mawunda awiri anjiwa kwa wansembe pa
khomo lolowera ku tenti ya msonkhano. [11] Wansembe apereke imodzi
kuti ikhale nsembe yauchimo ndi ina nsembe yopsereza yotetezera
tchimo chifukwa anachimwa popezeka pafupi ndi mtembo. Ndipo tsiku
lomwelo apatulenso tsitsi la pamutu pake. [12] Adzipereke kwa Yehova pa
nthawi yodzipatula ndipo abweretse nkhosa yayimuna ya chaka chimodzi
ngati nsembe yopepesera. Masiku akale sawerengedwanso chifukwa
anadzidetsa pa nthawi yodzipatulira kwake.

[13] “Tsono ili ndi lamulo la Mnaziri pamene nthawi yodzipatula kwake
yatha: Abwere naye pa khomo la tenti ya msonkhano. [14] Pamenepo
apereke chopereka chake kwa Yehova: Nkhosa yayimuna ya chaka chi-
modzi yopanda chilema kuti ikhale nsembe yopsereza, mwana wankhosa
wamkazi mmodzi wopanda chilema kuti ikhale nsembe yauchimo,
ndi nkhosa imodzi yayikulu yayimuna kuti ikhale nsembe yachiyan-
jano, [15] ndipo abwere pamodzi ndi nsembe yachakudya ndi nsembe
yachakumwa ndi dengu la buledi wopanda yisiti, makeke opangidwa ndi
ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta, ndi timitanda ta buledi topakidwa
mafuta.

[16] “Wansembe apereke zimenezi pamaso pa Yehova ndi kuchita nsembe
ya uchimo ndi nsembe yopsereza. [17] Apereke dengu la buledi wopanda
yisiti ndiponso nsembe yachiyanjano kwa Yehova ya nkhosa yayimuna,
pamodzi ndi chopereka cha chakudya ndi chopereka cha chakumwa.

[18] “Mnaziriyo amete tsitsi limene analipereka lija pa khomo la tenti
ya msonkhano. Atenge tsitsilo ndi kuliyika pa moto umene uli pansi pa
nsembe yachiyanjano.

19 "Mnaziriyo atatha kumeta tsitsi analiperekalo, wansembe ayike
m'manja mwake mwendo wa mmwamba wankhosa yayimuna umene
waphikidwa ndipo atengenso keke ndi kamtanda ka buledi, zonse zopanda
yisiti zomwe zili m'dengu lija. 20 Wansembe aziweyule pamaso pa
Yehova ngati nsembe yoweyula. Zimenezi ndi zopatulika ndipo ndi
za wansembe pamodzi ndi chidale chimene anachiweyula ndi ntchafu
yomwe anayipereka ija. Zitatha izi, Mnaziri akhoza kumwa vinyo.
21 "Ili ndi lamulo la Mnaziri yemwe walonjeza kudzipereka kwa Yehova
podzipatula yekha kuphatikiza pa zomwe angathe kukwaniritsa. Ayenera
kukwaniritsa lonjezo lomwe wachitalo potsata lamulo la Mnaziri."

### *Kupereka Mdalitso*

22 Yehova anawuza Mose kuti, 23 "Uza Aaroni ndi ana ake aamuna kuti,
'Umu ndi mmene muzidalitsira Aisraeli. Muzinena kuti,
24 " 'Yehova akudalitse
ndi kukusunga;
25 Yehova awalitse nkhope yake pa iwe,
nakuchitira chisomo;
26 Yehova akweze nkhope yake pa iwe,
nakupatse mtendere.' "
27 Choncho akadzatchula dzina langa podalitsa Aisraeli, Ine ndidza-
wadalitsadi.

## 7

### *Zopereka Popatula Chihema*

1 Mose atamaliza kuyimika chihema chija, anachidzoza mafuta ndi
kuchipatula pamodzi ndi ziwiya zake zonse. Anadzozanso guwa lansembe
ndi kulipatula pamodzi ndi ziwiya zake zonse. 2 Kenaka atsogoleri a
Aisraeli, akuluakulu a mabanja omwe ankayang'anira mafuko a anthu
omwe anawawerenga aja, anachita chopereka. 3 Anabweretsa zopereka
zawo pamaso pa Yehova: ngolo zophimbidwa zisanu ndi imodzi ndiponso
ng'ombe zothena khumi ndi ziwiri. Mtsogoleri mmodzi ng'ombe yothena
imodzi ndipo atsogoleri awiri ngolo imodzi. Izi anazipereka ku chihema.
4 Yehova anawuza Mose kuti, 5 "Ulandire zimenezi kwa iwo kuti zigwire
ntchito ku tenti ya msonkhano. Uzipereke kwa Alevi, aliyense monga mwa
ntchito yake."
6 Choncho Mose anatenga ngolo ndi ng'ombe zothenazo nazipereka kwa
Alevi. 7 Anapereka ngolo ziwiri ndi ng'ombe zothena zinayi kwa Ageresoni
monga mwantchito yawo 8 ndiponso anapereka ngolo zinayi ndi ng'ombe
zothena zisanu ndi zitatu kwa Amerari molingananso ndi ntchito yawo.
Onsewa ankawayang'anira anali Itamara mwana wa Aaroni wansembe.
9 Koma Mose sanapereke zimenezi kwa Akohati chifukwa zinthu zawo
zopatulika zomwe ankayang'anira zinali zoti azinyamula pa mapewa awo.
10 Guwa la nsembe litadzozedwa, atsogoleri anabweretsa zopereka zawo
zopatulira guwa nazipereka paguwapo. 11 Pakuti Yehova anawuza Mose
kuti, "Tsiku lililonse mtsogoleri mmodzi azibweretsa chopereka chake
chopatulira guwa lansembe."

12 Amene anabweretsa chopereka chake tsiku loyamba anali Naasoni
mwana wa Aminadabu wa fuko la Yuda.
13 Chopereka chake chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilogalamu
imodzi, ndi beseni lasiliva limodzi lowazira, lolemera magalamu 800,

zonse monga mwa muyeso wa ku malo wopatulika ndipo zonse
ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta ngati
chopereka chachakudya; 14 mbale imodzi yagolide yolemera magalamu
110, yodzaza ndi lubani; 15 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi,
nkhosa yayimuna imodzi ndi mwana wankhosa wamwamuna mmodzi
wa chaka chimodzi, za nsembe yopsereza; 16 mbuzi yayimuna imodzi,
nsembe ya machimo; 17 ndi ng'ombe zothena ziwiri, nkhosa zazimuna
zisanu, mbuzi zazimuna zisanu ndi ana ankhosa asanu a chaka chimodzi
kuti zikhale za nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha
Naasoni mwana wa Aminadabu.

18 Pa tsiku lachiwiri, Natanieli mwana wa Zuwara, mtsogoleri wa Isakara,
anabweretsa chopereka chake.
19 Chopereka chomwe anabwera nacho chinali mbale imodzi yasiliva
yolemera kilogalamu imodzi, beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera
magalamu 800, molingana ndi muyeso wa ku malo opatulika. Mbale
zonse zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta monga
chopereka cha chakudya. 20 Mbale imodzi yagolide yolemera magalamu
110 yodzaza ndi lubani; 21 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi,
nkhosa yayimuna imodzi ndi mwana wankhosa mmodzi wa chaka
chimodzi, za nsembe yopsereza: 22 mbuzi yayimuna imodzi ya nsembe
yotetezera machimo; 23 ndi ng'ombe ziwiri, nkhosa zazimuna ziwiri,
mbuzi zazimuna zisanu ndi ana ankhosa asanu a chaka chimodzi,
nsembe ya chiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Netanieli mwana wa
Zuwara.

24 Pa tsiku lachitatu, Eliabu mwana wa Heloni, mtsogoleri wa Azebuloni,
anabweretsa chopereka chake.
25 Chopereka chake chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilogalamu
imodzi ndi theka, ndi beseni limodzi lasiliva lowazira lolemera magalamu 800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika, mbale
zonse zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta, chopereka
cha chakudya; 26 mbale imodzi yagolide yolemera magalamu 110,
yodzaza ndi lubani; 27 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi,
nkhosa yayimuna imodzi ndi mwana wankhosa wamwamuna mmodzi
wa chaka chimodzi, za nsembe yopsereza; 28 mbuzi imodzi ya nsembe
yopepesera machimo; 29 ndi ng'ombe ziwiri, nkhosa zazimuna zisanu,
mbuzi zazimuna zisanu ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka
chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Eliabu
mwana wa Heloni.

30 Tsiku lachinayi linali la Elizuri mwana wa Sedeuri, mtsogoleri wa fuko
la Rubeni, anabweretsa chopereka chake.
31 Chopereka chake chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilogalamu
imodzi ndi theka, beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera magalamu
800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika; zonse ziwiri
zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta, chopereka
chachakudya. 32 Mbale imodzi yagolide yolemera magalamu 110, yodzaza ndi lubani; 33 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi, nkhosa
yayimuna imodzi ndi mwana wankhosa wa chaka chimodzi, za nsembe
yopsereza; 34 mbuzi imodzi ya nsembe yopepesera machimo; 35 ndi
ng'ombe zazimuna ziwiri, nkhosa zazimuna ziwiri, mbuzi zazimuna

zisanu ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Elizuri mwana wa Sedeuri.

36 Pa tsiku lachisanu Selumieli mwana wa Zurisadai, mtsogoleri wa fuko la Simeoni, anabweretsa chopereka chake.

37 Chopereka chake chinali mbale yasiliva yolemera kilogalamu imodzi ndi theka ndi beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera magalamu 800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika. Zonse ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta monga chopereka chachakudya;
38 mbale yagolide imodzi yolemera 110, yodzaza ndi lubani;
39 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi, nkhosa imodzi ndi mwana wankhosa mmodzi wamwamuna wa chaka chimodzi, za nsembe yopsereza;
40 mbuzi imodzi ya nsembe yopepesera machimo;
41 ng'ombe ziwiri, nkhosa zisanu, mbuzi zazimuna zisanu ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Selumieli mwana wa Zurisadai.

42 Pa tsiku lachisanu ndi chimodzi, Eliyasafu mwana wa Deuweli, mtsogoleri wa fuko la Gadi, anabweretsa chopereka chake.

43 Chopereka chakecho chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilogalamu imodzi ndi theka, beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera magalamu 800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika; zonse ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta monga chopereka chachakudya;
44 mbale imodzi yagolide yolemera magalamu 110, yodzaza ndi lubani;
45 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi, nkhosa yayimuna imodzi ndi mwana wankhosa wamwamuna mmodzi wa chaka chimodzi, chopereka cha nsembe yopsereza:
46 mbuzi yayimuna imodzi ya nsembe yopepesera machimo;
47 ng'ombe zazimuna ziwiri, nkhosa zazimuna zisanu, mbuzi zazimuna zisanu ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Eliyasafu mwana wa Deuweli.

48 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri Elisama mwana wa Amihudi, mtsogoleri wa fuko la Efereimu, anabweretsa chopereka chake.

49 Chopereka chakecho chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilogalamu imodzi ndi theka, ndi beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera magalamu 800, zonsezi monga mwa muyeso wa ku malo opatulika, zonse ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta monga chopereka chachakudya;
50 mbale imodzi yagolide yolemera magalamu 110, yodzaza ndi lubani;
51 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi, nkhosa imodzi yayimuna ndi mwana wankhosa wamwamuna mmodzi wa chaka chimodzi, nsembe yopsereza;
52 mbuzi imodzi ya nsembe yopepesera machimo;
53 ng'ombe ziwiri, nkhosa zazimuna zisanu, mbuzi zazimuna zisanu ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Elisama mwana wa Amihudi.

54 Pa tsiku lachisanu ndi chitatu Gamalieli mwana wa Pedazuri, mtsogoleri wa fuko Manase, anabweretsa chopereka chake.

55 Chopereka chakecho chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilogalamu imodzi ndi theka, ndi beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera magalamu 800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika;

zonse ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta
monga chopereka chachakudya; 56 mbale imodzi yagolide yolemera
magalamu 110, yodzaza ndi lubani, 57 mwana wang'ombe wamwamuna
mmodzi, nkhosa yayimuna imodzi ndi mwana wankhosa mmodzi
wa chaka chimodzi, nsembe yopsereza; 58 mbuzi imodzi ya nsembe
yopepesera machimo; 59 ng'ombe zazimuna ziwiri, nkhosa zazimuna
zisanu, mbuzi zazimuna zisanu ndi ana ankhosa a chaka chimodzi,
nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Gamalieli mwana wa
Pedazuri.

60 Pa tsiku lachisanu ndi chinayi Abidani mwana wa Gideoni mtsogoleri
wa fuko la Benjamini, anabweretsa chopereka chake.

61 Chopereka chakecho chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilo-
galamu imodzi ndi theka ndi beseni limodzi lowazira lolemera mag-
alamu 800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika; zonse
ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta monga
chopereka cha zakudya; 62 mbale imodzi yagolide yolemera magalamu
110, yodzaza ndi lubani; 63 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi,
nkhosa imodzi yayimuna ndi mwana wankhosa mmodzi wa chaka
chimodzi, nsembe yopsereza; 64 mbuzi yayimuna imodzi ya nsembe
yopepesera machimo; 65 ng'ombe zazimuna ziwiri, nkhosa zazimuna
zisanu, mbuzi zazimuna zisanu, ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka
chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Abidani
mwana wa Gideoni.

66 Pa tsiku lakhumi Ahiyezeri mwana wa Amisadai, mtsogoleri wa fuko la
Dani anabweretsa chopereka chake.

67 Chopereka chake chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilogalamu
imodzi ndi theka, beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera magalamu
800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika, zonse ziwiri zinali
zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta monga chopereka
chachakudya; 68 mbale imodzi yagolide yolemera magalamu 110, yo-
dzaza ndi lubani; 69 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi, nkhosa
imodzi yayimuna ndi mwana wankhosa mmodzi wa chaka chimodzi,
nsembe yopsereza; 70 mbuzi yayimuna imodzi ya nsembe yopepesera
machimo; 71 ndi ng'ombe ziwiri zazimuna, nkhosa zazimuna zisanu,
mbuzi zazimuna zisanu, ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka
chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Ahiyezeri
mwana wa Amisadai.

72 Pa tsiku la khumi ndi chimodzi, Pagieli mwana wa Okirani, mtsogoleri
wa fuko la Aseri, anabweretsa chopereka chake.

73 Chopereka chakecho chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilo-
galamu imodzi ndi theka, beseni limodzi lowazira lasiliva lolemera
magalamu 800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo opatulika; zonse
ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta monga
chopereka chachakudya; 74 mbale imodzi yagolide yolemera magalamu
110, yodzaza ndi lubani; 75 mwana wang'ombe wamwamuna mmodzi,
nkhosa imodzi yayimuna ndi mwana wankhosa mmodzi wa chaka
chimodzi, za nsembe yopsereza; 76 mbuzi imodzi yayimuna ya nsembe
yopepesera machimo; 77 ng'ombe ziwiri zazimuna, nkhosa zazimuna

zisanu, mbuzi zazimuna zisanu, ndi ana ankhosa aamuna asanu a chaka chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali chopereka cha Pagieli mwana wa Okirani.

78 Pa tsiku la khumi ndi chimodzi Ahira mwana wa Enani, mtsogoleri wa fuko la Nafutali, anabweretsa chopereka chake.

79 Chopereka chakecho chinali mbale imodzi yasiliva yolemera kilo-
galamu imodzi ndi theka, beseni limodzi lowazira lasiliva lowazira
lolemera magalamu 800, zonse monga mwa muyeso wa ku malo
opatulika, zonse ziwiri zinali zodzaza ndi ufa wosalala wosakaniza
ndi mafuta monga chopereka chachakudya; 80 mbale imodzi yagolide
yolemera magalamu 110, yodzaza ndi lubani; 81 mwana wang'ombe
wamwamuna mmodzi, nkhosa imodzi yayimuna ndi mwana wankhosa
mmodzi wa chaka chimodzi, nsembe yopsereza; 82 mbuzi yayimuna
imodzi ya nsembe yopepesera machimo; 83 ng'ombe zazimuna ziwiri,
nkhosa zazimuna zisanu, mbuzi zazimuna zisanu, ndi ana ankhosa
aamuna asanu a chaka chimodzi, nsembe yachiyanjano. Ichi chinali
chopereka cha Ahira mwana wa Enani.

84 Zopereka za atsogoleri a Israeli zopatulira guwa lansembe pamene
linadzozedwa zinali izi: mbale khumi ndi ziwiri zasiliva, mabeseni
owazira asiliva khumi ndi awiri ndi mbale zagolide khumi ndi ziwiri.
85 Mbale iliyonse yasiliva inkalemera kilogalamu imodzi ndi theka, ndipo
beseni lililonse lowazira linkalemera magalamu 800. Pamodzi, mbale
zonse zasiliva zinkalemera makilogalamu 27 monga mwa muyeso wa
ku malo opatulika. 86 Mbale khumi ndi ziwiri zagolide zodzaza ndi
lubanizo zinkalemera magalamu 110 iliyonse, monga mwa muyeso wa
ku malo opatulika. Pamodzi, mbale zagolide zinkalemera kilogalamu
imodzi ndi theka. 87 Chiwerengero cha nyama zonse za nsembe yopsereza
chinali motere: ng'ombe zazimuna khumi ndi ziwiri, nkhosa zazimuna
khumi ndi ziwiri ndi ana ankhosa aamuna khumi ndi awiri a chaka
chimodzi pamodzi ndi chopereka chachakudya. Mbuzi zazimuna khumi
ndi ziwiri zinali za nsembe yopepesera machimo. 88 Chiwerengero cha
nyama zonse za nsembe yachiyanjano chinali motere: ng'ombe zothena
24, nkhosa zazimuna 60, mbuzi zazimuna 60 ndi ana ankhosa aamuna a
chaka chimodzi 60. Zimenezi ndi zimene zinali zopereka zopatulira guwa
lansembe litadzozedwa.

89 Mose atalowa mu tenti ya msonkhano kukayankhula ndi Yehova, anamva mawu kuchokera pakati pa Akerubi awiri amene anali pamwamba pa chivundikiro cha bokosi la umboni. Ndipo anayankhula naye.

# 8

*Za Nyale*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Yankhula ndi Aaroni kuti pamene
uyimika nyale zisanu ndi ziwiri, nyalezo ziziyaka kutsogolo kwa choyikapo
nyale."

3 Aaroni anachitadi zomwezo. Anayimika nyale ndi kuziyang'anitsa
kumene kunali choyikapo nyale monga Yehova analamulira Mose.
4 Choyikapo nyalecho chinapangidwa motere: chinasulidwa kuchokera
ku golide, kuyambira pa tsinde pake mpaka ku maluwa ake. Choyikapo
nyalecho chinapangidwa monga momwe Yehova anaonetsera Mose.

*Za Kupatulidwa kwa Alevi*

[5] Yehova anawuza Mose kuti, [6] “Tenga Alevi pakati pa Aisraeli ndipo
uwayeretse. [7] Powayeretsa uchite izi: uwawaze madzi oyeretsa ndipo
amete thupi lawo lonse ndi kuchapa zovala zawo kuti adziyeretse. [8] Atenge
ng’ombe yayimuna yaying’ono ndi chopereka cha chakudya cha ufa
wosalala wosakaniza ndi mafuta. Atengenso ng’ombe ina yayimuna,
yaying’ono, ya chopereka chopepesera machimo. [9] Ubwere nawo Aleviwo
kutsogolo kwa tenti ya msonkhano ndipo usonkhanitse gulu la Aisraeli.
[10] Ubwere nawo pamaso pa Yehova, ndipo Aisraeli asanjike manja awo
pa iwo. [11] Aaroni apereke Alevi aja pamaso pa Yehova ngati chopereka
choweyula kuchokera kwa Aisraeli kuti akhale okonzeka kugwira ntchito
ya Yehova.

[12] “Alevi akatsiriza kusanjika manja awo pa mitu ya ng’ombe zaz-
imuna, imodzi ikhale ya nsembe yopepesera machimo ndipo inayo ikhale
ya nsembe yopsereza ya kwa Yehova, kupepesera machimo a Alevi.
[13] Uyimiritse Aleviwo pamaso pa Aaroni ndi ana ake aamuna ndipo
uwapereke ngati nsembe yoweyula kwa Yehova. [14] Pochita zimenezi
mudzapatula Alevi pakati pa Aisraeli ndipo Aleviwo adzakhala anga.

[15] “Utatha kuyeretsa ndi kupereka Aleviwo monga nsembe yoweyula,
apite kukagwira ntchito yawo ku tenti ya msonkhano. [16] Iwo ndiwo
Aisraeli amene aperekedwa kwathunthu kwa Ine. Ndawatenga kuti akhale
anga m’malo mwa mwana wamwamuna aliyense woyamba kubadwa wa
Mwisraeli aliyense wamkazi. [17] Mwana aliyense wamwamuna woyamba
kubadwa mu Israeli, kaya wa munthu kapena wa ziweto, ndi wanga.
Pamene ndinakantha ana oyamba kubadwa ku Igupto, ndinawapatulira
kwa Ine mwini. [18] Ndipo ndatenga Alevi m’malo mwa ana aamuna onse
oyamba kubadwa mu Israeli. [19] Mwa Aisraeli onse, ndapereka Alevi kuti
akhale mphatso kwa Aaroni ndi ana ake aamuna kugwira ntchito ya ku
tenti ya msonkhano m’malo mwa Aisraeli onse kuti azikapereka nsembe
yopepesera machimo, kuti mliri usadzaphe Aisraeli pamene ayandikira ku
malo wopatulika.”

[20] Mose, Aaroni pamodzi ndi gulu lonse la Israeli anachita kwa Alevi
monga momwe Yehova analamulira Mose. [21] Alevi anadziyeretsa ndi
kuchapa zovala zawo. Kenaka Aaroni anawapereka ngati nsembe
yoweyula pamaso pa Yehova ndi kuchita nsembe yopepesera machimo
yowayeretsa. [22] Zitatha zimenezi, Alevi anapita kukagwira ntchito yawo
ku tenti ya msonkhano motsogozedwa ndi Aaroni ndi ana ake aamuna.
Anachita kwa Alevi monga momwe Yehova analamulira Mose.

[23] Yehova anawuza Mose kuti, [24] “Ntchito za Alevi ndi izi: Amuna a
zaka 24 kapena kuposera pamenepa ndiye azibwera kudzagwira ntchito
ku tenti ya msonkhano. [25] Koma akakwana zaka makumi asanu, apume pa
ntchito yawo ya tsiku ndi tsiku ndi kulekeratu kugwira ntchitoyo. [26] Atha
kuthandiza abale awo kugwira ntchito za ku tenti ya msonkhano, koma
iwowo asamagwire ntchitoyo. Mmenemu ndimo ugawire ntchito yomwe
azigwira Alevi.”

# 9

*Paska*

[1] Yehova anayankhula ndi Mose m’chipululu cha Sinai pa mwezi
woyamba wa chaka chachiwiri atatuluka mu Igupto, nati, [2] “Aisraeli
azichita Paska pa nthawi yake yoyikika. [3] Muzichita Paska pa nthawi

yake yoyikika, madzulo a tsiku la 14 la mwezi uno, potsata malamulo ndi
malangizo ake.”

4 Choncho Mose anawuza Aisraeli kuti azichita Paska, 5 ndipo anachitadi
Paskayo m’chipululu cha Sinai madzulo a tsiku la 14 la mwezi woyamba.
Aisraeli anachita zonse monga momwe Yehova analamulira Mose.

6 Koma ena a iwo sanathe kuchita nawo Paska pa tsiku limenelo
chifukwa anali odetsedwa chifukwa chokhudza mtembo. Choncho
anabwera kwa Mose ndi Aaroni tsiku lomwelo, 7 ndipo anawuza Moseyo
kuti, “Ife tadetsedwa chifukwa cha mtembo wa munthu. N’chifukwa
chiyani taletsedwa kupereka nsembe kwa Yehova pamodzi ndi Aisraeli
ena pa nthawi yake?”

8 Mose anawayankha kuti, “Dikirani mpaka nditamva zimene Yehova
walamula zokhudza Inu.”

9 Ndipo Yehova anawuza Mose kuti, 10 “Uza Aisraeli kuti, ‘Pamene wina
mwa inu kapena zidzukulu zanu adetsedwa chifukwa chokhudza mtembo
wa munthu, kapena akakhala pa ulendo, akhoza kuchita nawo Paska ya
Yehova. 11 Azichita chikondwererochi madzulo a pa tsiku la 14 la mwezi
wachiwiri. Azidya mwana wankhosa wamwamuna pamodzi ndi buledi
wopanda yisiti ndi ndiwo zowawa zamasamba. 12 Iwo asasiye nyama
ina iliyonse mpaka mmawa. Asaswe mafupa aliwonse. Pamene akuchita
chikondwerero cha Paska, atsate malangizo onse. 13 Koma ngati munthu
wina ali woyeretsedwa ndipo sali pa ulendo koma alephera kuchita Paska,
munthu ameneyo achotsedwe pakati pa anthu a mtundu wake chifukwa
sanabweretse chopereka cha Yehova pa nthawi yake. Munthu ameneyo
adzalangidwa chifukwa cha tchimo lake.

14 “ ‘Mlendo amene akukhala pakati panu, nafuna kuchita nawo Paska
ya Yehova, achite nawo motsata malamulo ndi malangizo ake. Muzikhala
ndi malangizo ofanana a Paska; mbadwa kapena mlendo.’ ”

### *Mtambo Pamwamba pa Chihema*

15 Pa tsiku limene anayimika chihema, tenti ya umboni, mtambo
unaphimba chihemacho. Kuyambira madzulo mpaka mmawa, mtambo
umene unali pamwamba pa chihemacho unkaoneka ngati moto.
16 Zinkachitika motere mosalekeza: mtambo unkakhala pamwamba pa
chihema, ndipo usiku unkaoneka ngati moto. 17 Nthawi ina iliyonse
mtambo ukachoka pamwamba pa chihema, Aisraeli ankasamukanso,
ndipo paliponse pamene mtambo wayima, Aisraeli ankamangapo misasa.
18 Aisraeli ankasamuka pamalopo Yehova akawalamula, ndipo ankaman-
ganso misasa Iyeyo akawalamula. Nthawi yonse imene mtambowo way-
ima pa chihema, ankakhalabe m’misasa yawo. 19 Mtambowo ukakhala pa
chihema nthawi yayitali, Aisraeli ankasungabe lamulo la Yehova ndipo iwo
sankasamukanso. 20 Nthawi zina mtambowo unkakhala pa chihemapo
masiku owerengeka. Aisraeli ankamanga misasa molamulidwa ndi
Yehova ndipo ankasamukanso molamulidwa ndi Iyeyo. 21 Nthawi zina
mtambo unkakhala kuyambira madzulo mpaka mmawa ndipo unkachoka
mmawa mwake, ankasamuka. Kaya ndi masana kapena usiku, pamene
mtambo wachoka, ankasamuka. 22 Ngakhale mtambo ukhale pa chihema
masiku awiri kapena mwezi kapena chaka, Aisraeli ankakhalabe pa msasa
osachoka. Koma ukachoka, ankasamuka. 23 Molamulidwa ndi Yehova
ankamanga misasa yawo ndipo ankasamukanso Yehova akawalamula.
Ankamvera lamulo la Yehova kudzera mwa Mose.

# 10

### *Malipenga Asiliva*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 “Sula malipenga awiri a siliva, ndipo uzi-
wagwiritsa ntchito posonkhanitsa anthu pamodzi ndiponso powasamutsa
m’misasa. 3 Pamene akuliza malipenga onse awiri, anthu onse asonkhane
kwa iwe pa khomo la tenti ya msonkhano. 4 Akaliza limodzi lokha, atso-
goleri, akulu a mafuko a Aisraeli, asonkhane kwa iwe. 5 Akaliza lipenga
lochenjeza, misasa yomwe ili kummawa iyambe kusamuka. 6 Akaliza
lipenga lochenjeza lachiwiri, misasa yakummwera iyambe kusamuka.
Kuliza kwa lipenga lochenjeza kudzakhala chizindikiro choyamba ulendo.
7 Pofuna kusonkhanitsa anthu, muziliza malipenga, koma mosiyana ndi
mmene malipenga ochenjeza amalizidwira.

8 “Ana a Aaroni, ansembe aja, ndiwo aziliza malipengawo. Zimenezi
zikhale zokhazikika kwa inu ndi ku mibado yanu yonse. 9 Pamene
mukupita ku nkhondo m’dziko lanu lomwe, kulimbana ndi mdani amene
akukuzunzani, muziliza malipenga ochenjeza ndipo Yehova Mulungu
wanu adzakukumbukirani ndi kukulanditsani m’manja mwa adani anu.
10 Komanso pa nthawi yanu ya chisangalalo, pa maphwando anu oyikika
ndi maphwando a mwezi watsopano, muziliza malipenga pa nsembe zanu
zopsereza ndi nsembe zanu za chiyanjano, ndipo zidzakhala chikumbutso
chanu pamaso pa Mulungu. Ine ndine Yehova Mulungu wanu.”

### *Aisraeli Achoka ku Sinai*

11 Pa chaka chachiwiri, mwezi wachiwiri, tsiku la 20, mtambo unachoka
pamwamba pa chihema cha umboni. 12 Ndipo Aisraeli ananyamuka ku-
choka m’chipululu cha Sinai ndipo anayenda malo osiyanasiyana mpaka
pamene mtambo unayima m’chipululu cha Parani. 13 Kameneka kanali
koyamba kuti Aisraeli anyamuke monga momwe Yehova analamulira
Mose.

14 Magulu a msasa wa Yuda ndiwo anayamba kunyamuka potsata
mbendera yawo. Mtsogoleri wa gulu lawo anali Naasoni mwana wa
Aminadabu. 15 Mtsogoleri wa gulu la fuko la Isakara anali Netanieli
mwana wa Zuwara, 16 Eliabu mwana wa Heloni ndiye anali mtsogoleri
wa fuko la Zebuloni. 17 Kenaka anagwetsa chihema, ndipo Ageresoni ndi
Amerari amene ananyamula chihemacho, ananyamuka.

18 Kenaka magulu a msasa wa fuko la Rubeni ananyamuka potsatira
mbendera yawo. Mtsogoleri wawo anali Elizuri mwana wa Sedeuri.
19 Mtsogoleri wa fuko la Simeoni anali Selumieli mwana wa Zurisadai,
20 ndipo Eliyasafu mwana wa Deuweli ndiye ankatsogolera fuko la Gadi.
21 Kenaka Akohati ananyamuka atanyamula zinthu zopatulika. Chihema
chinkayenera kuyimikidwa iwo asanafike.

22 Magulu a msasa wa Aefereimu anatsatira potsatira mbendera yawo.
Elisama mwana wa Amihudi ndiye anali mtsogoleri wawo. 23 Gamalieli
mwana wa Pedazuri ndiye anali mtsogoleri wa fuko la Manase. 24 Abidani
mwana wa Gideoni ndiye anali mtsogoleri wa mtundu wa Benjamini.

25 Pambuyo pa magulu onse panali magulu a msasa wa Dani, omwe
ankateteza magulu onsewa ndipo ananyamuka potsatira mbendera yawo.
Mtsogoleri wawo anali Ahiyezeri mwana wa Amisadai. 26 Pagieli mwana
wa Okirani ndiye anali mtsogoleri wa fuko la Aseri, 27 ndipo mtsogoleri
wa mtundu wa Nafutali anali Ahira mwana wa Enani. 28 Umenewu

ndiwo unali mndandanda wa kayendedwe ka magulu a Aisraeli pamene
ankanyamuka ulendo wawo m'magulumagulu.
29 Ndipo Mose anawuza Hobabu mwana wa Reueli Mmidiyani, mpon-
gozi wa Mose kuti, "Tikunyamuka kupita ku malo amene Yehova anati,
'Ndidzakupatsani.' Tiye upite nafe ndipo tidzakusamalira bwino, pakuti
Yehova analonjeza zinthu zabwino kwa Israeli."
30 Hobabu anayankha kuti, "Ayi, sindipita nanu, ndibwerera ku dziko la
kwathu ndi kwa abale anga."
31 Ndipo Mose anati, "Pepa usatisiye popeza ukudziwa kumene tinga-
mange misasa m'chipululu muno ndipo udzakhala maso athu. 32 Iweyo
ukapita nafe, tidzagawana nawe zinthu zabwino zomwe Yehova adzati-
patsa."
33 Motero ananyamuka ku Phiri la Yehova nayenda ulendo wa masiku
atatu. Bokosi la Chipangano cha Yehova linkayenda patsogolo pawo pa
masiku atatuwo kuti apeze malo woti apumulepo. 34 Mtambo wa Yehova
unkawaphimba masana pamene ankasamuka pa misasa yawo.
35 Nthawi iliyonse imene Bokosi la Chipangano likunyamuka, Mose
ankanena kuti,

"Dzukani, Inu Yehova!
Adani anu abalalike;
Odana nanu athawe pamaso panu.

36 "Pamene likupumula, ankanena kuti,

"Bwererani, Inu Yehova,
ku chinamtindi cha Aisraeli."

# 11

### *Moto Wochokera kwa Yehova*

1 Anthu atadandaula kwa Yehova chifukwa cha mavuto awo, Yehovayo
anamva ndipo anakwiya kwambiri. Kenaka moto wa Yehova unayaka
pakati pawo ndi kutentha zigawo zina za kunja kwa msasa. 2 Anthuwo
analira kwa Mose ndipo Moseyo atapemphera kwa Yehova, motowo
unazima. 3 Motero malowo anawatcha Tabera, chifukwa moto wa Yehova
unayaka pakati pawo.

### *Zinziri Zochokera kwa Yehova*

4 Anthu ena osokoneza amene anali pakati pa Aisraeli anayamba
kukhumba chakudya cha ku Igupto ndipo Aisraeli nawonso anayamba
kufuwula kwambiri n'kumati, "Tikanangopeza nyama yoti n'kudya!
5 Tikukumbukira nsomba zaulere zimene tinkadya ku Igupto komanso
nkhaka, mavwende, anyezi wamitundumitundu ndi adyo. 6 Koma tsopano
chilakolako chathu chatha. Sitikuona kanthu kena kakudya koma mana
basi!"
7 Mana ankafanana ndi mbewu zamapira ndipo maonekedwe ake anali
ngati ulimbo wowuma. 8 Anthu ankapita kukatola manawo, n'kumasinja
mu mtondo kapena kupera. Ankawaphika mu m'phika kapena kupanga
makeke. Ndipo ankakoma ngati makeke ophikira mafuta a olivi. 9 Mame
akamagwa pa msasawo usiku ankagwera kumodzi ndi manawo.
10 Mose anamva anthu a banja lililonse akufuwula, banja lililonse pa
khomo la tenti yake. Yehova anakwiya kwambiri ndipo Mose anavu-
tikanso mu mtima. 11 Mose anafunsa Yehova kuti, "Chifukwa chiyani
mwabweretsa mavuto otere pa mtumiki wanune? N'chiyani chimene
ndachita choti sichinakusangalatseni mpaka kundisenzetsa katundu wa

anthu onsewa? 12 Kodi Ndine amene ndinatenga pathupi pa anthu
onsewa? Kodi ndinawabala ndine? Bwanji mukundiwuza kuti ndiwanya-
mule m'manja mwanga, monga momwe mlezi amanyamulira kamwana,
kupita nawo ku malo omwe munalonjeza ndi lumbiro kwa makolo awo?
13 Ndingayipeze kuti nyama yoti anthu onsewa adye? Iwowa akulirira
ine kuti, 'Tipatse nyama tidye!' 14 Sindingathe kusamala anthu onsewa
ndekha. Katundu ameneyu ndi wolemera kwambiri kwa ine. 15 Ngati
umu ndi mmene muzichitira nane, chonde ingondiphani pompano. Koma
ngati mwandikomera mtima ndiye ndisaonenso mavutowa."

16 Yehova anawuza Mose kuti, "Undibweretsere anthu 70 ochokera
pakati pa akuluakulu a Aisraeli, amene umawadziwa kuti ndiwo atsogoleri
komanso akuluakulu a mabanja. Abwere ku tenti ya msonkhano kuti
ayime kumeneko pamodzi ndi iwe. 17 Ndidzatsika ndi kuyankhula
nawe kumeneko, ndipo ndidzatenga mzimu umene uli pa iwe ndi
kuyika pa iwowo. Adzakuthandiza kusenza nkhawa za anthuwa ndipo
sudzasenzanso wekha."

18 "Uwawuze anthuwo kuti, 'Mudziyeretse, kukonzekera mawa, pamene
mudzadya nyama.' Yehova anakumvani pamene munkalira kuti,
'Zikanakhala bwino tikanapeza nyama yoti tidye! Tinkakhala bwino ku
Igupto!' Tsopano Yehova adzakupatsani nyama ndipo mudzayidyadi.
19 Simudzadya tsiku limodzi lokha, kapena masiku awiri, kapena asanu,
khumi kapena masiku makumi awiri, 20 koma mwezi wonse, mpaka
itakukolani ndi kutopa nayo chifukwa mwakana Yehova yemwe ali pakati
panu ndipo mwalira pamaso pake kuti, 'Bwanji tinachoka ku Igupto?' "

21 Koma Mose anati, "Taonani pano ndili pakati pa anthu 600,000 amene
ndi kuyenda nawo ndipo Inuyo mukuti, 'Ndidzawapatsa nyama kuti
adye mwezi wathunthu!' 22 Kodi ngakhale titapha nkhosa ndi ng'ombe,
zingawakwanire? Ngakhale titagwira nsomba zonse za m'nyanja, kodi
zingawakwanire iwowa?"

23 Yehova anayankha Mose kuti, "Kodi dzanja langa ndi lalifupi? Uwona
tsopano ngati zimene ndanenazo zichitike kapena ayi."

24 Choncho Mose anatuluka nakawuza anthu zomwe Yehova ana-
nena. Anasonkhanitsa pamodzi akuluakulu makumi asanu ndi awiri
aja ndi kuwayimiritsa mozungulira Chihema. 25 Ndipo Yehova anatsika
m'mitambo ndi kuyankhula naye ndipo anatengako mzimu womwe unali
pa Mose ndi kuwuyika pa akuluakulu makumi asanu ndi awiri aja.
Pamene mzimuwo unakhazikika pa akuluakuluwo, anayamba kunenera
koma sanapitirize.

26 Koma anthu ena awiri omwe mayina awo anali Elidadi ndi Medadi,
anatsalira mu msasa. Anali nawo m'gulu la olembedwa aja, koma sanapite
nawo ku Chihema. Komabe mzimu unakhala pa iwo ndipo ananenera
ali mu msasa. 27 Mnyamata wina anathamanga kudzawuza Mose kuti,
"Elidadi ndi Medadi akunenera mu msasa."

28 Yoswa mwana wa Nuni, mtumiki wa Mose kuyambira ubwana wake,
anayankha kuti, "Mbuye wanga Mose, aletseni!"

29 Koma Mose anati, "Kodi ukuchita nsanje chifukwa cha ine?
Ndikanakonda kuti anthu onse a Yehova akhale aneneri ndi kuti Yehova
ayike mzimu wake pa iwo!" 30 Mose ndi akuluakulu a Israeli aja
anabwerera ku msasa.

31 Pamenepo Yehova anawutsa mphepo yochokera ku nyanja imene in-
abweretsa zinziri. Zinzirizo zinagwera pansi kuzungulira msasa, mtunda
wa kilomita imodzi mbali zonse ndipo msinkhu wake unali mita imodzi.

32 Tsiku limenelo masana onse mpaka usiku ndiponso tsiku lotsiralo,
anthu anatuluka kunja kukatola zinziri. Palibe amene anasonkhanitsa
zochepera makilogalamu 1,000 ndipo anaziyanika kuzungulira msasa
wonse. 33 Koma pamene anthuwo ankadya nyamayo, asanayimeze
n'komwe, ukali wa Yehova unafika pa iwo ndipo Iye anawakantha ndi
mliri woopsa. 34 N'chifukwa chake malowo anawatcha Kibiroti Hatava
chifukwa pamenepo anakwirirapo anthu osusuka aja.

35 Kuchoka pa Kibiroti Hatava anthuwo anayenda kupita ku Heziroti
ndipo anakhala kumeneko kwa kanthawi.

# 12

*Miriamu ndi Aaroni Atsutsana ndi Mose*

1 Miriamu ndi Aaroni anayamba kuyankhula motsutsana ndi Mose
chifukwa cha mkazi wa ku Kusi, popeza Moseyo anakwatira Mkusi.
2 Iwowo anafunsa kuti, "Kodi Yehova anayankhula kudzera mwa Mose
yekha? Kodi sanayankhule kudzeranso mwa ife?" Ndipo Yehova anamva
zimenezi.

3 (Koma Mose anali munthu wodzichepetsa kwambiri kuposa munthu
aliyense pa dziko lapansi).

4 Nthawi yomweyo Yehova anati kwa Mose, Aaroni ndi Miriamu,
"Bwerani ku tenti ya msonkhano nonse atatu." Ndipo atatuwo anapitadi
kumeneko. 5 Tsono Yehova anatsika mu mtambo, nayima pa khomo la
chihema. Kenaka anayitana Aaroni ndi Miriamu. Ndipo onse awiri atapita
patsogolo, 6 Mulungu anati, "Mverani mawu anga:
"Pakakhala mneneri wa Yehova pakati panu,
ndimadzionetsera kwa iyeyo m'masomphenya,
ndimayankhula naye m'maloto.
7 Koma sinditero ndi Mose mtumiki wanga;
Iyeyu ndi wokhulupirika m'nyumba yanga yonse.
8 Ndimayankhula naye maso ndi maso,
momveka bwino osati mophiphiritsa;
ndipo amaona maonekedwe a Yehova.
N'chifukwa chiyani simunaope
kuyankhula motsutsana ndi Mose mtumiki wanga?"

9 Ndipo Yehova anawakwiyira, nachoka.

10 Pamene mtambo unachoka pamwamba pa Chihema, taonani, Miri-
amu anagwidwa ndi khate. Aaroni atachewuka anaona Miriamu ali
ndi khate; 11 ndipo Aaroni anawuza Mose kuti, "Pepani mbuye wanga,
musatilange chifukwa cha tchimo limene tachita mopusa. 12 Musalole kuti
Miriamu akhale ngati mwana wobadwa wakufa kuchoka m'mimba mwa
amayi ake, thupi lake litawonongeka."

13 Tsono Mose anafuwulira Yehova kuti, "Chonde Inu Mulungu, muchir-
itseni!"

14 Yehova anayankha Mose kuti, "Abambo ake akanamulavulira malovu
m'maso, kodi sakanakhala wonyozeka masiku asanu ndi awiri? Mut-
sekereni kunja kwa msasa masiku asanu ndi awiri, kenaka mumulowet-
senso." 15 Choncho anamutsekera Miriamu kunja kwa msasa masiku
asanu ndi awiri ndipo anthu sanayende ulendo wawo mpaka Miriamu
atamulowetsanso.

16 Pambuyo pake anthu ananyamuka ku Heziroti ndi kukamanga
m'chipululu cha Parani.

# 13

*Kukazonda Kanaani*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 “Tuma anthu kuti akazonde dziko la
Kanaani limene ndikupereka kwa Aisraeli. Kuchokera pa fuko lililonse
utume munthu mmodzi amene ndi mtsogoleri wawo.”

3 Monga mwa mawu a Yehova, Mose anawatuma kuchokera ku
chipululu cha Parani. Onsewo anali atsogoleri a Aisraeli. 4 Mayina awo
ndi awa:

kuchokera ku fuko la Rubeni, Samuwa mwana wa Zakuri;
5 kuchokera ku fuko la Simeoni, Safati mwana wa Hori;
6 kuchokera ku fuko la Yuda, Kalebe mwana wa Yefune;
7 kuchokera ku fuko la Isakara, Igala mwana wa Yosefe;
8 kuchokera ku fuko la Efereimu, Hoseya mwana wa Nuni;
9 kuchokera ku fuko la Benjamini, Paliti mwana wa Rafu;
10 kuchokera ku fuko la Zebuloni, Gadieli mwana wa Sodi;
11 kuchokera ku fuko la Manase (fuko la Yosefe), Gadi mwana wa Susi;
12 kuchokera ku fuko la Dani, Amieli mwana wa Gemali;
13 kuchokera ku fuko la Aseri, Seturi mwana wa Mikayeli;
14 kuchokera ku fuko la Nafutali, Naabi mwana wa Vofisi;
15 kuchokera ku fuko la Gadi, Geuweli mwana wa Maki.

16 Amenewa ndiwo mayina a anthu amene Mose anawatuma kukazonda
dzikolo. (Hoseya mwana wa Nuni, Mose anamupatsa dzina loti Yoswa).

17 Mose atawatuma kuti akazonde Kanaani anati, “Mupite kudzera ku
Negevi, mukapitirire mpaka ku dziko la mapiri. 18 Mukaone dzikolo kuti
ndi lotani ndi anthu okhala m’menemo ngati ndi amphamvu kapena
ofowoka, ochepa kapena ambiri. 19 Nanga dziko limene akukhalako ndi
lotani? Ndi labwino kapena loyipa? Mizinda imene akukhalamo ndi
yotani? Kodi ilibe malinga kapena ndi ya malinga? 20 Nthaka yake
ndi yotani? Yachonde kapena yopanda chonde? Kodi dzikolo lili ndi
mitengo kapena lilibe mitengo? Mukayesetse kubweretsako zipatso za
m’dzikomo.” (Inali nthawi yamphesa zoyamba kupsa).

21 Choncho anapita kukazonda dzikolo kuchokera ku chipululu cha Zini
mpaka ku Rehobu, mopenyana ndi Lebo Hamati. 22 Anapita kudzera ku
Negevi ndi kukafika ku Hebroni, kumene Ahimani, Sesai ndi Talimai, ana a
Anaki ankakhala. (Anamanga Hebroni zaka zisanu ndi ziwiri asanamange
Zowani ku Igupto). 23 Atafika ku chigwa cha Esikolo, anadulako nthambi
ya mpesa ya phava limodzi la mphesa ndipo anthu awiri ananyamulizana,
natenganso makangadza ndi nkhuyu. 24 Malo amenewo anawatcha
chigwa cha Esikolo chifukwa cha phava la mphesa limene Aisraeli anadula
kumeneko. 25 Patapita masiku makumi anayi, anthu aja anabwerako
kokazonda dziko lija.

*Kufotokoza Zomwe Anakaona*

26 Ndipo atabwerako anapita kwa Mose ndi Aaroni ndi kwa Aisraeli
onse ku Kadesi m’chipululu cha Parani. Kumeneko anafotokozera anthu
onse nawaonetsanso zipatso za m’dzikolo. 27 Anthuwo anafotokozera
Mose kuti, “Tinapita ku dziko komwe munatituma. Dzikolo ndi loyenda
mkaka ndi uchi ndipo zipatso zake ndi izi. 28 Koma anthu amene

amakhala m'dzikomo ndi amphamvu, mizinda yawo ndi ya malinga
aakulu kwambiri. Tinaonanso Aanaki kumeneko. 29 Aamaleki amakhala
ku Negevi, Ahiti, Ayebusi ndi Aamori amakhala m'dziko la mapiri ndipo
Akanaani amakhala pafupi ndi nyanja, m'mbali mwa Yorodani."

30 Koma Kalebe anawakhalitsa chete anthuwo pamaso pa Mose, ndipo
anati, "Tiyeni tipite ndithu ndi kutenga dzikolo, pakuti tingathe kulitenga."

31 Koma anthu aja amene anapita naye anati, "Sitingathe kulimbana
ndi anthuwo popeza ndi amphamvu kuposa ifeyo." 32 Choncho anthuwo
anafalitsa pakati pa Aisraeli mbiri yoyipa ya dziko lomwe anakalionalo.
Iwo anati, "Dziko limene tinapita kukalizonda limawononga anthu okhala
m'menemo. Ndipo anthu onse amene tinakawaona kumeneko ndi
ataliatali. 33 Kumeneko tinaona Anefili (ana a Aanaki ochokera kwa
Nefili). Ifeyo timangodziona ngati ziwala m'maso mwawo, ndipo kwa iwo
timaonekadi motero ndithu."

# 14

*Anthu Awukira*

1 Usiku umenewo gulu lonse la Aisraeli linalira mofuwula kwambiri.
2 Ndipo Aisraeli onse anayankhula motsutsana ndi Mose ndi Aaroni. Gulu
lonse linanena kwa iwo kuti, "Kunali bwino tikanafera ku Igupto kapena
m'chipululu muno! 3 N'chifukwa chiyani Yehova akutilowetsa m'dziko
limenelo? Kodi kuti tikaphedwe ndi lupanga? Kuti akazi ndi ana athu
akatengedwe ngati katundu wolanda ku nkhondo? Kodi sikungakhale
bwino kuti tibwerere ku Igupto?" 4 Ndipo anawuzana wina ndi mnzake
kuti, "Tiyeni tisankhe mtsogoleri ndipo tibwerere ku Igupto."

5 Koma Mose ndi Aaroni anadzigwetsa pansi chafufumimba pamaso
pa Aisraeli onse omwe anasonkhana pamenepo. 6 Yoswa mwana wa
Nuni ndi Kalebe mwana wa Yefune, omwe anali amodzi mwa amene
anakazonda nawo dziko, anang'amba zovala zawo 7 ndipo anati kwa gulu
lonse la Aisraeli, "Dziko limene tinakayendamo ndi kuliona ndi labwino
kwambiri zedi. 8 Ngati Yehova akukondwera nafe, adzatitsogolera kulowa
m'dziko limenelo. Dziko loyenda mkaka ndi uchi adzalipereka kwa ife,
9 koma musawukire Yehova. Komanso musaope anthu a m'dzikomo,
pakuti tidzawagonjetsa. Chitetezo chawachokera, koma ife Yehova ali
nafe. Musawaope."

10 Koma gulu lonse linayankhula zofuna kuwagenda miyala. Pamenepo
ulemerero wa Yehova unaonekera kwa Aisraeli onse ku tenti ya
msonkhano. 11 Yehova anawuza Mose kuti, "Anthu awa adzandinyoza
mpaka liti? Sadzandikhulupirira mpaka liti, ngakhale ndachita zizindikiro
zozizwitsa zonsezi pakati pawo? 12 Ndidzawakantha ndi mliri ndi
kuwawononga. Koma ndidzakusandutsa iwe mtundu waukulu ndi
wamphamvu kuposa iwo."

13 Mose anati kwa Yehova, "Aigupto adzamva zimenezi! Mwa mphamvu
yanu munawatulutsa anthu amenewa pakati pawo. 14 Ndipo iwowo
adzawuza anthu okhala m'dziko lino zimenezi. Anthuwa amva kale kuti
Inu Yehova mumakhala pakati pa anthu amenewa ndi kuti Inuyo Yehova
mwawaonekera maso ndi maso. Mtambo wanu umakhala pamwamba
pawo ndiponso mumayenda nawo mu mtambo woyima, masana ndi
moto woyima, usiku. 15 Tsono mukawapha anthu onsewa nthawi imodzi,
mayiko amene anamva za Inu adzati, 16 'Yehova walephera kuwalowetsa

anthuwo m'dziko lomwe anawalonjeza molumbira, ndipo wawapha
m'chipululu.'

17 "Chonde Ambuye wonetsani mphamvu yanu monga munalonjezera
kuti, 18 'Yehova sakwiya msanga, ndipo ndi wodzaza ndi chikondi
chosasinthika, wokhululukira tchimo ndi kuwukira. Koma Iye sadzaleka
kulanga ochimwa. Iyeyo amalanga ana chifukwa cha tchimo la makolo
awo kufikira m'bado wachitatu ndi wachinayi.' 19 Chifukwa cha kukula
kwa chikondi chanu chosasinthika, akhululukireni anthuwa tchimo lawo
monga mwakhala mukuwakhululukira kuchokera pa nthawi imene ana-
choka ku Igupto mpaka tsopano."

20 Yehova anayankha kuti, "Ndawakhululukira monga wapemphera.
21 Komabe, ndikunenetsa kuti pali Ine, ndiponso pamene dziko lapansi
ladzaza ndi ulemerero wa Yehova, 22 palibe ndi mmodzi yemwe mwa
anthu amene anaona ulemerero wanga ndi zizindikiro zozizwitsa zimene
ndinazichita ku Igupto ndi m'chipululu muno, koma osandimvera ndi
kundiyesa kokwanira kakhumi, 23 palibe ndi mmodzi yemwe wa anthu
amenewa amene adzaone dziko limene ndinalonjeza ndi lumbiro kwa
makolo awo. Aliyense amene anandinyoza sadzaliona dzikolo. 24 Koma
mtumiki wanga Kalebe, pakuti ali ndi mtima wosiyana ndi ena ndiponso
amanditsatira ndi mtima wonse, ndidzamulowetsa m'dziko limene anapi-
tamolo ndipo zidzukulu zake zidzalandira dzikolo ngati cholowa chawo.
25 Ndipo popeza kuti Aamaleki ndi Akanaani akukhala ku chigwa, mawa
mubwerere ndipo mupite ku chipululu podzera ku Nyanja Yofiira."

26 Yehova anawuza Mose ndi Aaroni kuti, 27 "Kodi anthu oyipawa
adzang'ung'udza ndi kutsutsana nane mpaka liti? Ndamva madandawulo
a Aisraeli ong'ung'udzawa. 28 Tsono awuze kuti, 'Ndikulumbira pali
Ine,' akutero Yehova, 'Ndidzakuchitirani zinthu zonse zimene ndamva inu
mukunena: 29 Mitembo yanu idzakhala ili ngundangunda m'chipululu
muno; mtembo wa munthu aliyense pakati panu amene ali ndi zaka
makumi awiri kapena kupitirirapo, amene anawerengedwa pa chiw-
erengero chija ndipo anang'ung'udza motsutsana nane. 30 Palibe ndi
mmodzi yemwe mwa inu amene adzalowe m'dziko lomwe ndinalumbira
mokweza manja kuti likhale lanu, kupatula Kalebe mwana wa Yefune
ndi Yoswa mwana wa Nuni. 31 Koma ana anu amene mukunena kuti
adzatengedwa ngati katundu wolanda ku nkhondo, Ine ndidzawalowetsa
kuti akasangalale m'dziko limene munalikana. 32 Koma inu mitembo
yanu idzakhala ngundangunda m'chipululu muno. 33 Ana anu adza-
khala abusa m'chipululu muno zaka makumi anayi, kuvutika chifukwa
cha kusakhulupirika kwanu, mpaka munthu womaliza mwa inu atafa
m'chipululu muno. 34 Mudzavutika chifukwa cha machimo anu kwa
zaka makumi anayi Chaka chimodzi chikuyimira tsiku limodzi la masiku
makumi anayi amene munakazonda dziko lija ndipo mudzadziwa kuyipa
kwake kwa kukangana ndi Ine.' 35 Ine Yehova, ndanena, ndidzachitadi
zimenezi kwa anthu onse oyipawa, amene agwirizana kunditsutsa.
Adzathera m'chipululu momwe muno, adzafera muno basi."

36 Ndipo anthu amene Mose anawatuma kukazonda dziko aja anachoka
pamaso pake nachititsa gulu lonse la anthu kuwukira Moseyo chifukwa
chofalitsa mbiri yoyipa ya dzikolo. 37 Anthu amene ankafalitsa mbiri
yoyipa ya dzikolo anakanthidwa ndi mliri ndipo anafa pamaso pa Yehova.
38 Mwa anthu amene anakaona dzikolo, Yoswa mwana wa Nuni ndi Kalebe
mwana wa Yefune ndi okhawo amene anapulumuka.

39 Mose atafotokoza izi kwa Aisraeli onse, anthuwo analira kwambiri.
40 Mmamawa tsiku linalo anapita mbali ya ku dziko la mapiri. Iwo anati,
"Tachimwa, tipita ku dziko limene Yehova anatilonjeza."

41 Koma Mose anati, "Chifukwa chiyani simukumvera lamulo la Yehova?
Zimenezi sizitheka! 42 Musapite chifukwa Yehova sali pakati panu.
Mudzagonjetsedwa ndi adani anu 43 chifukwa kumeneko mukakumana
ndi Aamaleki ndi Akanaani. Popeza mwaleka kutsata Yehova, Iyeyo
sadzakhala nanu ndipo mudzaphedwa ndi lupanga."

44 Komabe mwa maganizo awo anapita molunjika dziko la mapiri
ngakhale kuti Mose sanachoke ndi Bokosi la Chipangano la Yehova pa
msasa. 45 Koma Aamaleki ndi Akanaani amene ankakhala ku dziko
lamapirilo anatsika ndi kumenyana nawo ndipo anawakantha m'njira
yonse mpaka ku Horima.

# 15

*Zopereka Zapadera*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Yankhula ndi Aisraeli ndipo uwawuze
kuti, 'Mukakalowa m'dziko limene ndikukupatsanilo, 3 ndipo mukamadza-
pereka kwa Yehova, nsembe yotentha pa moto ya ng'ombe kapena
nkhosa monga fungo lokoma kwa Yehova, kaya ndi nsembe yopsereza
kapena nsembe zina, nsembe yapadera chifukwa cha lumbiro kapena
nsembe yoperekedwa mwaufulu kapenanso yoperekedwa pa chikondw-
erero, 4 munthu amene akubweretsa zopereka zake, azikapereka kwa
Yehova chopereka chachakudya cholemera kilogalamu imodzi ya ufa
wosalala wosakaniza ndi mafuta wokwana lita imodzi. 5 Pamodzi ndi
mwana wankhosa aliyense wa nsembe yopsereza kapena nsembe ina,
muzikakonzanso lita imodzi la vinyo ngati chopereka cha chakumwa.' "

6 "Pamodzi ndi nkhosa yayimuna, muzikakonzanso chopereka cha
chakudya cholemera makilogalamu awiri a ufa wosalala, wosakaniza ndi
mafuta okwanira lita imodzi ndi theka, 7 ndi vinyo wokwanira lita imodzi
ndi theka ngati chopereka cha chakumwa. Muzikapereka monga nsembe
yopereka fungo lokoma kwa Yehova.

8 " 'Pamene mukukonza mwana wang'ombe wamwamuna kuti akhale
nsembe yopsereza kapena nsembe ina iliyonse: ya lumbiro lapadera
kapena nsembe yachiyanjano kwa Yehova, 9 pamodzi ndi mwana
wang'ombe wamwamunayo muzibweretsa nsembe yachakudya yolemera
makilogalamu atatu a ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta okwana malita
awiri. 10 Komanso muzibweretsa vinyo wokwanira malita awiri monga
chopereka chachakumwa. Imeneyi idzakhala chopereka chotentha pa
moto kuti likhale fungo lokoma kwa Yehova. 11 Ng'ombe yayimuna
iliyonse kapena nkhosa yayimuna iliyonse, mwana wankhosa aliyense
kapena mbuzi yaying'ono, zizikonzedwa motere. 12 Ngakhale zingachu-
luke chotani, chitani izi kwa iliyonse ya nyamazo.

13 " 'Mbadwa iliyonse ya mu Israeli izichita zimenezi pamene ibweretsa
nsembe yotentha pa moto kuti ikhale fungo lokoma kwa Yehova. 14 Ku
mibado yanu yonse ya m'tsogolo, pamene mlendo kapena wina aliyense
wokhala pakati panu apereka chopereka chotentha pa moto kuti chikhale
fungo lokoma kwa Yehova, azichita mofanana ndi momwe inu mumachi-
tira. 15 Gulu lonse likhale ndi malamulo ofanana a inu kapena mlendo
wokhala pakati panu. Limeneli ndi lamulo lamuyaya kwa mibado imene

ikubwera. Inuyo ndi mlendo mudzakhala wofanana pamaso pa Yehova.
[16] Mudzakhale ndi malamulo ndi miyambo yofanana, inuyo ndi mlendo
wokhala pakati panu.' "
[17] Yehova anawuza Mose kuti, [18] "Yankhula ndi Aisraeli ndipo un-
ene kuti, 'Mukakalowa m'dziko limene ndikukutengeraniko [19] ndipo
mukakadya chakudya cha m'dzikolo, mukapereke gawo lina kwa Yehova
monga chopereka. [20] Pa buledi wanu woyamba, mukapereke mmodzi
monga nsembe, ngati chopereka chochokera ku malo wopunthira tirigu.
[21] Pa mibado yanu yonse muzidzapereka chopereka ichi kwa Yehova
kuchokera ku zakudya zanu zoyamba za m'nthaka.

### *Chopereka Chopepesera Machimo Ochita Mosadziwa*

[22] " 'Ndipo ngati muchimwa mosadziwa posasunga ena mwa malamulo
awa amene Yehova wapereka kwa Mose, [23] lina lililonse mwa malamulo
a Yehova amene wapereka kwa inu kudzera mwa Mose, kuyambira
tsiku limene Yehova anawapereka mpaka mibado ya m'tsogolo, [24] ndipo
ngati zimenezi zachitika osati mwadala ndipo gulu lonse silinadziwe,
zikatero gulu lonselo lipereke mwana wang'ombe wamwamuna monga
nsembe yopsereza kuti likhale fungo lokoma kwa Yehova pamodzinso
ndi chopereka chachakudya ndi chopereka cha chakumwa ndi mbuzi
yayimuna ngati nsembe yopepesera machimo potsata zimene zinala-
mulidwa. [25] Wansembe apereke nsembe yopepesera machimo a gulu
lonse la Aisraeli, ndipo adzakhululukidwa, pakuti linali tchimo lochita
mosadziwa. Ndipo chifukwa cha tchimo lawolo, abweretse kwa Yehova
nsembe yotentha pa moto ndi nsembe yopepesera machimo. [26] Gulu lonse
la Aisraeli ndi alendo okhala pakati pawo adzakhululukidwa chifukwa
anthu onsewo anachimwa mosadziwa.
[27] " 'Koma ngati munthu mmodzi achimwa mosadziwa, ayenera kubw-
eretsa mbuzi yayikazi ya chaka chimodzi kuti ikhale nsembe yopepesera
machimo. [28] Wansembe apereke nsembe yopepesera machimowo pamaso
pa Yehova chifukwa cha munthu yemwe anachimwa mosadziwayo.
Nsembe yopepesera tchimo lakelo ikaperekedwa, munthuyo adzakhulu-
lukidwa. [29] Lamulo lomweli ligwiritsidwe ntchito kwa aliyense wochimwa
mosadziwa, kaya ndi mbadwa ya mu Israeli kapena mlendo.
[30] " 'Koma aliyense amene achimwa mwadala, kaya ndi mbadwa kapena
mlendo, nachitira chipongwe Yehova, ameneyo achotsedwe ndithu pakati
pa anthu ake. [31] Popeza wanyoza mawu a Yehova ndi kuphwanya
malamulo ake. Munthu ameneyo achotsedwe ndithu, kuchimwa kwake
kudzakhala pa iyeyo.' "

### *Wosasunga Sabata Aphedwa*

[32] Aisraeli ali m'chipululu, munthu wina anapezeka akutola nkhuni
tsiku la Sabata. [33] Amene anamupeza akutola nkhunizo anabwera
naye kwa Mose ndi Aaroni ndi kwa gulu lonse [34] ndipo anamutsekera
m'ndende chifukwa sankadziwa choti achite naye. [35] Pamenepo Yehova
anawuza Mose kuti, "Munthu ameneyu ayenera kuphedwa. Gulu lonse
liyenera kumugenda ndi miyala kunja kwa msasa." [36] Choncho gululo
linamutengera kunja kwa msasa ndi kumupha pomugenda ndi miyala,
monga momwe Yehova analamulira Mose.

### *Mphonje pa Zovala*

[37] Yehova anawuza Mose kuti, [38] "Yankhula ndi Aisraeli ndipo uwawuze
kuti, 'Pa mibado yanu yonse muzisokerera mphonje pa ngodya za zovala

zanu ndipo pa ngodya ya mphonje iliyonse azisokererapo chingwe chobiri-
wira. 39 Mudzakhala ndi mphonje zimenezi kuti mukaziona muzikakum-
bukira malamulo onse a Yehova ndi kuwamvera kuti musamatsatenso
zilakolako za m'mitima mwanu ndi za maso anu. 40 Motero mudzakum-
bukira kumvera malamulo anga ndipo mudzakhala opatulikira a Mulungu
wanu. 41 Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene ndinakutulutsani
m'dziko la Igupto kuti ndikhale Mulungu wanu. Ine ndine Yehova
Mulungu wanu.' "

# 16

*Kora, Datani ndi Abiramu Awukira Mose*

1 Kora mwana wa Izihari, mwana wa Kohati, mwana wa Levi ndi Datani
ndi Abiramu ana a Eliabu, pamodzi ndi Oni mwana wa Perezi, ana a
Rubeni, anayamba kudzikuza, 2 ndipo anawukira Mose. M'gulu mwawo
munali atsogoleri a Aisraeli 250, anthu otchuka amene anasankhidwa ndi
anthu pa msonkhano. 3 Iwo anasonkhana kudzatsutsana ndi Mose ndi
Aaroni nawawuza kuti, "Mwawonjeza! Anthu onsewa ndi oyera, aliyense
wa iwo, ndipo Yehova ali pakati pawo. Chifukwa chiyani mukudzikuza
pakati pa gulu lonse la Yehova?"

4 Mose atamva izi, anagwa chafufumimba. 5 Ndipo iye anawuza
Kora ndi anthu onse amene ankamutsatira kuti, "Yehova mawa mmawa
adzasonyeza yemwe ndi wake ndiponso amene ndi woyera mtima.
Munthuyo adzabwera pafupi ndi Iye. Munthu amene adzamusankheyo
adzamusendeza pafupi. 6 Iwe Kora pamodzi ndi onse amene akukutsatira
chitani izi: Tengani zofukizira 7 ndipo mawa muyikemo moto ndi lubani
pamaso pa Yehova. Munthu amene Yehova amusankhe ndiye amene ali
woyera. Alevi inu mwawonjeza kwambiri!"

8 Mose anawuzanso Kora kuti, "Inu Alevi, tsopano tamverani! 9 Kodi
sizinakukwanireni kuti Mulungu wa Israeli anakupatulani pakati pa gulu
lonse la Aisraeli ndi kukubweretsani pafupi ndi Iye, kuti muzigwira ntchito
ku nyumba ya Yehova ndi kumayima pamaso pa gulu, kumatumikira?
10 Wakubweretsa iwe pamodzi ndi Alevi anzako kufupi ndi Iye mwini.
Koma tsopano ukufuna kutenganso unsembe. 11 N'kulakwira Yehova kuti
iwe ndi gulu lako lonseli mwasonkhana kuti mutsutsane ndi Yehova. Kodi
Aaroni ndani kuti muzikangana naye?"

12 Kenaka Mose anayitana Datani ndi Abiramu, ana aamuna a Eliabu
koma iwo anati, "Sitibwera! 13 Kodi sikukwanira kuti unatitulutsa,
kutichotsa m'dziko loyenda mkaka ndi uchi kuti udzatiphe m'chipululu
muno? Kodi tsopano ukufunanso kutilemetsa? 14 Kuwonjezera apo,
sunatilowetse m'dziko loyenda mkaka ndi uchi kapena kutipatsa malo
wolima ndi minda ya mpesa. Kodi ukufuna kuchotsa maso a anthuwa?
Ayi, sitibwera!"

15 Pamenepo Mose anakwiya kwambiri ndipo anati kwa Yehova, "Musa-
landire chopereka chawo. Sindinatenge kalikonse kwa iwo ngakhale bulu,
ndiponso sindinalakwire wina aliyense wa iwo."

16 Mose anati kwa Kora, "Iwe ndi okutsatira onse mudzaonekere pamaso
pa Yehova mawa, iweyo ndi iwowo pamodzi ndi Aaroni. 17 Munthu
aliyense akatenge chofukizira ndi kuyikamo lubani, zofukizira 250 zonse
pamodzi ndi kuzibweretsa pamaso pa Yehova. Iwe ndi Aaroni mudz-
abweretsenso zofukizira zanu." 18 Choncho munthu aliyense anatenga
chofukizira chake nayikamo moto ndi lubani, ndipo anayima pamodzi

ndi Mose ndi Aaroni pa khomo la tenti ya msonkhano. 19 Kora
atasonkhanitsa omutsatira ake onse amene amatsutsa nawo pa khomo la
tenti ya msonkhano, ulemerero wa Yehova unaonekera kwa gulu lonselo.
20 Yehova anawuza Mose ndi Aaroni kuti, 21 "Chokani pakati pa gulu ili
kuti ndithetse mkanganowu kamodzin'kamodzi."

22 Koma Mose ndi Aaroni anadzigwetsa chafufumimba ndipo analira
mokweza, "Chonde Mulungu, Mulungu wa mizimu ya anthu onse, kodi
mudzakwiyira gulu lonse pamene munthu mmodzi yekha ndiye amene
wachimwa?"

23 Pamenepo Yehova anawuza Mose kuti, 24 "Uza gulu lonse kuti,
'Khalani kutali ndi matenti a Kora, Datani ndi Abiramu.' "

25 Mose anayimirira napita kwa Datani, Abiramu ndi kwa akuluakulu
a Israeli amene ankamutsatira. 26 Anachenjeza gulu lonse kuti, "Khalani
kutali ndi matenti a anthu oyipawa! Musakhudze kanthu kawo kalikonse,
mukatero mudzawonongedwa limodzi nawo chifukwa cha machimo
awo." 27 Choncho anthuwo anachokadi ku matenti a Kora, Datani ndi
Abiramu. Datani ndi Abiramu anali atatuluka nayima pamodzi ndi akazi
awo, ana awo ndi makanda awo pa makomo a matenti awo.

28 Tsono Mose anati, "Umu ndi mmene mudzadziwire kuti Yehova
ndiye amene ananditumа kuti ndichite zinthu zonsezi ndipo kuti si
maganizo anga. 29 Ngati anthu awa afa ndi imfa ya chilengedwe ndi
kuwachitikira zomwe zimachitikira munthu aliyense, ndiye kuti Yehova
sananditume. 30 Koma Yehova akachita china chake chachilendo, nthaka
nitsekula pakamwa pake ndi kuwameza iwo pamodzi ndi zonse zimene
ali nazo, iwowa n'kulowa m'manda ali moyo, pamenepo mudzazindikira
kuti anthu amenewa ananyoza Yehova."

31 Atangotsiriza kuyankhula zimenezi, nthaka ya pamene anayimapo
inagawikana 32 ndipo dziko linatsekula pakamwa pake ndi kuwameza
pamodzi ndi nyumba zawo ndi anthu onse a Kora ndi katundu wawo
yense. 33 Analowa m'manda amoyo pamodzi ndi zonse zimene anali nazo.
Nthaka inawatsekera ndi kuwawononga ndipo sanaonekenso. 34 Atamva
kulira kwawo, Aisraeli onse amene anali pafupi ndi anthuwo anathawa
akufuwula kuti, "Nthaka imezanso ife!"

35 Ndipo moto wochokera kwa Yehova unabwera n'kunyeketsa anthu
250 amene ankapereka nsembe yofukiza aja.

36 Yehova anawuza Mose kuti, 37 "Uza Eliezara mwana wa Aaroni,
wansembe kuti atenge zofukizirazo pakati pa mitembo yopsererayo
ndipo amwazire makalawo kutali chifukwa zofukizirazo n'zopatulika.
38 Izi ndi zofukizira za anthu omwe anafa chifukwa cha uchimo wawo.
Musule zofukizirazo kuti zikhale zophimbira pa guwa lansembe, chifukwa
zinaperekedwa kwa Yehova ndipo ndi zopatulika. Zimenezi zikhale
chizindikiro kwa Aisraeli."

39 Choncho Eliezara, wansembe, anasonkhanitsa zofukizira zamkuwa
zija zomwe anthu opsererawo anabwera nazo ndipo anazisula kuti zikhale
zophimbira pa guwa lansembe, 40 monga momwe Yehova anamulangizira
kudzera mwa Mose. Chimenechi chinali chikumbutso kwa Aisraeli kuti
munthu wina aliyense, kupatula zidzukulu za Aaroni, sayenera kupsereza
lubani pamaso pa Yehova, kuopa kuti munthu woteroyo angakhale ngati
Kora ndi omutsatira ake.

41 Tsiku lotsatira, gulu lonse la Aisraeli linatsutsana ndi Mose ndi Aaroni.
Iwo anati, "Inu mwapha anthu a Yehova."

[42] Koma pamene anthuwo anasonkhana kuti atsutsane ndi Mose ndi Aaroni, atatembenuka kuyang'ana ku tenti ya msonkhano, mwadzidzidzi mtambo unaphimba tentiyo ndipo ulemerero wa Yehova unaonekera.
[43] Pamenepo Mose ndi Aaroni anapita patsogolo pa tenti ya msonkhano
ija [44] ndipo Yehova anawuza Mose kuti, [45] "Chokani pakati pa gulu la anthuwa kuti ndiwawononge kamodzin'kamodzi." Ndipo iwo anagwa pansi chafufumimba.

[46] Kenaka Mose anawuza Aaroni kuti, "Tenga chofukizira chako ndipo ikamo lubani pamodzi ndi moto wochokera pa guwa lansembe, fulumira, pita pa gulu la anthuwo ndipo ukachite nsembe yopepesera machimo
awo popeza mkwiyo wa Yehova wafika, mliri wayamba." [47] Ndipo Aaroni anachita monga ananenera Mose, nathamangira m'katikati mwa gulu la anthuwo. Pamenepo n'kuti mliri utayamba kale pakati pa anthu aja ndipo Aaroni anafukiza lubani ndi kupereka nsembe yopepesera machimo awo.
[48] Iye anayimirira pakati pa anthu amoyo ndi akufa ndipo mliri unaleka.
[49] Komabe anthu 14, 700 anafa ndi mliriwo, kuwonjezera pa aja amene
anafa chifukwa cha Kora. [50] Ndipo Aaroni anabwerera kwa Mose ku khomo la tenti ya msonkhano, chifukwa mliriwo unali utatha.

# 17

*Kuphukira kwa Ndodo ya Aaroni*

[1] Yehova anawuza Mose kuti, [2] "Yankhula ndi Aisraeli ndipo akupatse ndodo khumi ndi ziwiri, imodzi kuchokera kwa mtsogoleri wa fuko
lililonse. Ulembe dzina la munthu aliyense pa ndodo yake. [3] Pa ndodo
ya Levi ulembepo dzina la Aaroni, chifukwa pafunika ndodo imodzi ya
mtsogoleri pa fuko lililonse. [4] Uyike ndodozo mu tenti ya msonkhano,
kutsogolo kwa Bokosi la Umboni, kumene ndimakumana nawe. [5] Ndodo
ya munthu amene ndamusankha idzachita maluwa potero ndidzaletsa madandawulo osatha a Aisraeli otsutsana nawe."

[6] Choncho Mose anayankhula ndi Aisraeli, ndipo atsogoleri awo anapereka ndodo khumi ndi ziwiri, imodzi kuchokera kwa mtsogoleri wa
fuko lililonse ndipo ndodo ya Aaroni inali pakati pa ndodo zawozo. [7] Mose
anayika ndodozo pamaso pa Yehova mu tenti ya msonkhano.

[8] Pa tsiku lotsatira Mose analowa mu tenti ya msonkhanoyo ndipo anaona kuti ndodo ya Aaroni, yomwe inkayimira fuko la Levi, sinangophuka masamba chabe, komanso inachita maluwa n'kubala zipatso za
alimondi. [9] Choncho Mose anatulutsa ndodo zonse pamaso pa Yehova napita nazo kwa Aisraeli onse. Iwowo anaziona ndipo munthu aliyense anatenga ndodo yake.

[10] Yehova anawuza Mose kuti, "Bwezera ndodo ya Aaroni patsogolo pa Bokosi la Umboni, kuti chikhale chizindikiro cha kuwukira kwawo. Zimenezi zidzathetsa kudandaula kwawo kotsutsana nane, kuopa kuti
angafe." [11] Mose anachita monga Yehova anamulamulira.

[12] Aisraeli anati kwa Mose, "Tikufa! Tatayika, tonse tatayika! [13] Aliyense
woyandikira chihema adzafa. Kodi ndiye kuti tonse tikufa?"

# 18

*Ntchito za Ansembe ndi Alevi*

[1] Yehova anawuza Aaroni kuti, "Iwe, ana ako aamuna ndi banja la abambo ako mudzasenza tchimo la malo wopatulika, koma iwe ndi

ana ako aamuna okha mudzasenza tchimo lokhudza unsembe wanu.
2 Ubweretse Alevi, abale ako, kuchokera ku fuko la abambo ako kuti
azikhala ndi iwe ndi kumakuthandiza pamodzi ndi ana ako amuna
pamene mukutumikira mu tenti ya umboni. 3 Iwowo azikutumikirani
ndipo azichita ntchito zonse za ku tenti, koma asamafike pafupi ndi
zipangizo za ku malo opatulika kapena guwa lansembe, kuopa kuti iwo
ndi inu mungafe. 4 Azikhala ndi inu ndipo azisamalira ntchito yonse ya
mu tenti ya msonkhano koma munthu wina aliyense wapadera sayenera
kufika pafupi nanu.

5 "Inuyo muzisamalira malo wopatulika ndi guwa lansembe, kuti ukali
wa Yehova usawagwerenso Aisraeli. 6 Ine mwini ndasankha Alevi, abale
ako, pakati pa Aisraeli ngati mphatso yako ndipo aperekedwa kwa Yehova
kuti azigwira ntchito ku tenti ya msonkhano. 7 Koma iwe wekha ndi
ana ako aamuna muzitumikira ngati ansembe ndi zina zonse zokhudza
pa guwa lansembe ndi za m'kati mwa malo wopatulika kwambiri.
Ndikukupatsani mphatso ya utumiki wa unsembe. Aliyense woyandikira
malo wopatulika ayenera kuphedwa.

### *Zopereka za Ansembe ndi Alevi*

8 "Kenaka Yehova anati kwa Aaroni, ona, Ine mwini ndikukuyika
kuti ukhale woyang'anira zopereka zobwera kwa Ine; zopereka zonse
zopatulika za Aisraeli zimene amapereka kwa ine ndi kuzipereka kwa iwe
ndi ana ako aamuna ngati gawo lanu la nthawi zonse. 9 Uzilandiranso
gawo la zopereka zopatulika kwambiri zomwe sizinawotchedwe pa
moto. Kuchokera pa mphatso zonse zimene amabweretsa kwa Ine ngati
zopatulika kwambiri, nsembe zachakudya kapena nsembe zopepesera
machimo, gawo limenelo ndi lako ndi ana ako aamuna. 10 Muzidya
zimenezo ngati zinthu zopatulika kwambiri; mwamuna aliyense adyeko.
Uzitenge kukhala zopatulika.

11 "Izinso ndi zako: chilichonse chopatulidwa kuchokera ku mphatso
zoweyula za Aisraeli ndapereka kwa iwe ndi ana ako aamuna ndi aakazi
ngati gawo lako la nthawi zonse. Aliyense wa m'nyumba mwako amene
ali woyeretsedwa monga mwa mwambo angathe kudyako.

12 "Ndikukupatsani mafuta onse abwino kwambiri a olivi ndi vinyo
yense watsopano wabwino kwambiri ndi tirigu yense zomwe Aisraeli
amapereka kwa Yehova ngati zipatso zoyamba pa zokolola zawo.
13 Zipatso zonse zoyamba kucha za m'dziko lawo zomwe amapereka
kwa Yehova zidzakhala zako. Aliyense m'nyumba mwako amene ali
woyeretsedwa angathe kudyako.

14 "Chilichonse mu Israeli chomwe chapatulidwira Yehova ndi chako.
15 Chilichonse choyamba kubadwa kwa munthu kaya nyama, chomwe
chaperekedwa kwa Yehova ndi chako. Koma uyenera kuwombola
mwana aliyense wamwamuna ndi mwana aliyense woyamba wa nyama
zodetsedwa. 16 Pamene zili ndi mwezi umodzi wa kubadwa, uziwombole
pa mtengo wowombolera wa ndalama zisanu zasiliva, monga mwa
ndalama za ku malo wopatulika.

17 "Koma usawombole ana oyamba kubadwa a ng'ombe, nkhosa kapena
mbuzi. Iwo ndi opatulika. Uwaze magazi a nyamazi pa guwa lansembe
ndi kutentha mafuta ake ngati nsembe yotentha ndi moto kuti likhale
fungo lokoma kwa Yehova. 18 Nyama yake ikhale yanu monga momwe
chimakhalira chidale cha nsembe yoweyula ndi ntchafu za miyendo ya
kumanja, zonsezi ndi zako. 19 Zonse zimene mwazichotsa ku zopereka

zoyera zomwe Aisraeli anapereka kwa Yehova ndazipereka kwa iwe ndi
ana ako aamuna ndi aakazi ngati gawo lanu nthawi zonse. Ili ndi pangano
losatha la mchere pamaso pa Yehova kwa iwe ndi ana ako."

20 Ndipo Yehova anati kwa Aaroni, "Iweyo sudzakhala ndi cholowa
m'dziko lawo, ndiponso sudzalandira gawo lililonse pakati pawo. Ine
ndine gawo lako ndi cholowa chako pakati pa Aisraeli.

21 "Taonani, ndawapatsa Alevi chakhumi chonse mu Israeli ngati
cholowa chawo chifukwa cha ntchito ya ku tenti ya msonkhano.
22 Kuyambira tsopano mpaka m'tsogolo Aisraeli asamapite pafupi ndi tenti
ya msonkhano. Ngati atero adzasenza zotsatira za tchimo lawo ndipo
adzafa. 23 Alevi ndi amene azidzagwira ntchito ya ku tenti ya msonkhano
ndipo adzalangidwa chilichonse chikalakwika. Ili ndi lamulo losatha kwa
mibado yawo yonse. Iwowo sadzalandira cholowa pakati pa Aisraeli.
24 M'malo mwake, ndikuwapatsa Aleviwo chakhumi ngati cholowa chawo
chimene Aisraeli amapereka kwa Yehova. N'chifukwa chake zokhudza
iwo ndinati: 'Sadzakhala ndi cholowa pakati pa Aisraeli.' "

25 Yehova anati kwa Mose, 26 "Yankhula ndi Alevi ndi kunena nawo
kuti, 'Pamene mulandira chakhumi kuchoka kwa Aisraeli chimene ndi-
makupatsani ngati cholowa chanu, muyenera kupereka chakhumi cha
choperekacho kwa Yehova. 27 Chopereka chanucho chidzawerengedwa
kwa inu ngati tirigu wochokera kopunthira kapena ngati mphesa zopsinya
kuchokera kopsinyira mphesa. 28 Mwa njira imeneyi inunso muzipereka
chopereka kwa Yehova kuchokera ku chakhumi chanu chilichonse
chimene mumalandira kuchokera kwa Aisraeli. Kuchokera ku chakhumi-
cho muziperekako gawo la Yehova kwa Aaroni, wansembe. 29 Muyenera
kupereka monga gawo la Yehova magawo abwino kwambiri ndi opatulika
a chilichonse chimene chapatsidwa kwa inu.'

30 "Nena kwa Alevi: 'Pamene mupereka gawo labwino lopambana
zonse, gawo limenelo lidzawerengedwa kwa inu ngati lochokera popun-
thira tirigu kapenanso kopsinyira mphesa. 31 Inu ndi a pa banja panu
mungathe kudyera zimenezi paliponse chifukwa ndi malipiro a ntchito
yanu ya ku tenti ya msonkhano. 32 Popereka gawo labwino kwambirilo
simudzapezeka olakwa. Mukatero simudzadetsa zopereka zoyera za
Aisraeli, ndipo simudzafa.' "

# 19

*Phulusa ndi Madzi Oyeretsera*

1 Yehova anati kwa Mose ndi Aaroni: 2 "Lamulo limene Yehova wapereka
ndi ili: Uzani Aisraeli kuti abweretse ng'ombe yayikazi yofiira yopanda
chilema chilichonse imenenso sinakhalepo pa goli. 3 Muyipereke kwa
Eliezara, wansembe ndipo apite nayo kunja kwa msasa. Iphedwe iye
ali pomwepo. 4 Ndipo Eliezara wansembe atengeko ena mwa magazi
a ng'ombeyo ndi chala chake ndi kuwaza kasanu n'kawiri ku tsogolo
kwa tenti ya msonkhano. 5 Wansembeyo akuona, ng'ombeyo ayiwotche
chikopa chake, mnofu wake, magazi ake ndi zam'kati zake. 6 Wansembe
atenge mtengo wamkungudza, hisope ndi kansalu kofiira ndipo aponye
zimenezo pakati pa moto umene akuwotchera ng'ombeyo. 7 Zitatha izi,
wansembeyo ayenera kuchapa zovala zake ndiponso asambe ndi madzi.
Iye angathe kupita ku msasa, komabe adzakhala wodetsedwa mpaka
madzulo. 8 Munthu amene amawotcha ng'ombeyo ayeneranso kuchapa

zovala zake ndi kusamba ndi madzi. Iyenso adzakhala wodetsedwa mpaka
madzulo.
9 “Munthu amene ndi woyeretsedwa achotse phulusa la ng’ombeyo ndi
kuliyika pa malo woyeretsedwa kunja kwa msasa. Aisraeli adzasunge
phulusalo kuti azikaligwiritsa ntchito polithira m’madzi woyeretsera
ndi wochotsera tchimo. 10 Munthu wochotsa phulusa la ng’ombeyo
ayeneranso kuchapa zovala zake. Iyenso adzakhala wodetsedwa mpaka
madzulo. Ili likhale lamulo la nthawi zonse kwa Aisraeli ndi alendo okhala
pakati pawo.
11 “Aliyense wokhudza mtembo wa munthu wina aliyense adzakhala
wodetsedwa masiku asanu ndi awiri. 12 Adziyeretse yekha ndi madzi pa
tsiku lachitatu ndi pa tsiku lachisanu ndi chiwiri ndipo adzayeretsedwa.
Koma ngati sadziyeretsa yekha pa tsiku la chitatu ndi lachisanu ndi
chiwiri sadzakhala woyeretsedwa. 13 Aliyense amene akhudza mtembo
wa munthu n’kulephera kudziyeretsa yekha, ndiye kuti wadetsa Nyumba
ya Yehova. Munthu ameneyo achotsedwe pakati pa Aisraeli. Iye ndi
wodetsedwa chifukwa sanamuwaze madzi oyeretsa; kudetsedwa kwake
kukhalabe pa iyeyo.
14 “Pamene munthu wamwalira mu tenti, lamulo lomwe ligwire ntchito
ndi ili: Aliyense wolowa mu tentimo ndi amene anali momwemo
adzakhala odetsedwa kwa masiku asanu ndi awiri, 15 ndiponso chiwiya
chilichonse chopanda chivundikiro chidzakhala chodetsedwa.
16 “Aliyense wokhudza munthu amene waphedwera kunja ndi lupanga
kapena amene wafa ndi imfa ya chilengedwe, kapena aliyense wokhudza
fupa la munthu kapena manda, munthu ameneyo adzakhala wodetsedwa
kwa masiku asanu ndi awiri.
17 “Za munthu wodetsedwayo: ikani phulusa lochokera ku nsembe ya
chiyeretso mu mtsuko ndi kuthiramo madzi abwino. 18 Tsono munthu
woyeretsedwa atenge hisope, amuviyike m’madzi ndi kuwaza tentiyo
ndi zipangizo zonse, pamodzi ndi anthu anali m’menemo. Ayenera
kuwazanso aliyense wakhudza fupa kapena, munthu wochita kuphedwa,
kapena amene wafa ndi imfa ya chilengedwe kapenanso amene wakhudza
manda. 19 Munthu woyeretsedwa ndiye awaze munthu wodetsedwayo
pa tsiku lachitatu ndi pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, ndipo pa tsiku
lachisanu ndi chiwiri amuyeretse. Munthu amene akuyeretsedwayo
ayenera kuchapa zovala zake ndi kusamba ndi madzi, ndipo madzulo
ake adzakhala woyeretsedwa. 20 Koma ngati munthu wodetsedwayo
sadziyeretsa yekha, ndiye kuti ayenera kuchotsedwa pakati pa gulu
chifukwa anadetsa malo wopatulika a Yehova, popeza sanawazidwe madzi
oyeretsa ndiye kuti ndi wodetsedwa. 21 Ili ndi lamulo lokhazikika kwa iwo.
“Munthu amene amawaza madzi oyeretsawo ayenera kuchapa zovala
zake ndipo yense wokhudza madzi oyeretserawo adzakhala wodetsedwa
mpaka madzulo. 22 Chilichonse chimene munthu wodetsedwayo
achikhudze chidzakhala chodetsedwa ndiponso aliyense wochikhudza
adzakhala wodetsedwa mpaka madzulo.”

# 20

*Madzi Ochokera M’thanthwe*

1 Pa mwezi woyamba gulu lonse la Aisraeli linafika ku chipululu cha Zini,
ndipo anakhala ku Kadesi. Miriamu anafera kumeneko ndipo anayikidwa
m’manda.

2 Kunalibe madzi woti anthu onse ndi kumwa, choncho anthuwo
anasonkhana motsutsana ndi Mose ndi Aaroni. 3 Anakangana ndi
Mose kuti, “Kunali bwino ifenso tikanangofa pamene abale athu anafa
pamaso pa Yehova! 4 Chifukwa chiyani unabweretsa gulu la Yehova
m’chipululu muno, kuti ife ndi ziweto zathu tife kuno? 5 N’chifukwa
chiyani unatitulutsa m’dziko la Igupto ndi kutibweretsa kumalo woyipa
ano? Kuno kulibe tirigu kapena nkhuyu, mphesa kapena makangadza.
Ndipo kuno kulibenso madzi akumwa!”

6 Mose ndi Aaroni anachoka mu msonkhano ndi kupita pa khomo la tenti
ya msonkhano, nagwa pansi chafufumimba ndipo ulemerero wa Yehova
unaonekera. 7 Yehova anati kwa Mose, 8 “Tenga ndodo, ndipo iwe ndi
m’bale wako Aaroni musonkhanitse anthu onse pamodzi. Uyankhule ndi
thanthwe ilo iwo akuona ndipo lidzatulutsa madzi ake. Udzatulutsa madzi
m’thanthwe limeneli kuti anthu onse ndi ziweto zawo amwe.”

9 Choncho Mose anatenga ndodo pamaso pa Yehova monga momwe
anamulamulira. 10 Mose ndi Aaroni anasonkhanitsa anthuwo pamodzi
ku thanthwelo ndipo Mose anawawuza kuti, “Tamverani osamvera inu,
kodi tikupatseni madzi kuchokera ku thanthwe ili?” 11 Choncho Mose
anatukula dzanja lake ndi kumenya thanthwelo kawiri ndi ndodo yake
ndipo madzi ambiri anatuluka mwamphamvu, ndipo anthu ndi ziweto
zawo anamwa.

12 Koma Yehova anati kwa Mose ndi Aaroni, “Chifukwa chakuti simu-
nandikhulupirire ndiponso simunandilemekeze monga Woyera pamaso
pa Aisraeli, simudzalowetsa anthuwa m’dziko limene ndikupereka kwa
iwo.”

13 Awa anali madzi a ku Meriba, kumene Aisraeli anakangana ndi
Yehova ndiponso kumene Yehovayo anadzionetsa yekha kuti ndi Woyera
pakati pawo.

### *Aedomu Akaniza Njira Aisraeli*

14 Mose anatumiza amithenga kuchokera ku Kadesi kupita kwa mfumu
ya ku Edomu, kukanena kuti,

“M’bale wako Israeli akunena izi: Inuyo mukudziwa za mavuto onse
amene anatigwera. 15 Makolo athu anapita ku Igupto ndipo tinakhala
kumeneko zaka zambiri. Aigupto anatizunza pamodzi ndi makolo
athuwo, 16 koma titalirira Yehova, Iyeyo anamva kulira kwathuko ndipo
anatitumizira mngelo amene anatitulutsa ku Igupto.”

“Taonani, tsopano tili pano pa Kadesi, mzinda wa m’malire a dziko
lanu. 17 Chonde mutilole tidutse m’dziko lanu. Sitidzera m’minda
yanu kapena mu mpesa wanu, kapenanso kumwa madzi m’chitsime
chilichonse. Tidzayenda kutsata msewu waukulu wa mfumu ndipo
sitidzapatukira ku dzanja lamanja kapena lamanzere mpaka titadutsa
malire a dziko lanu.”

18 Koma Edomu anayankha kuti,

“Musadutse kuno: Mukangoyesera tidzabwera ndi kumenyana nanu
ndi lupanga.”

19 Aisraeli anayankha kuti,

“Tidzayenda motsata msewu waukulu. Ndipo ngati ife kapena ziweto
zathu tidzamwa madzi anu tidzalipira. Tikungofuna tidutse nawo,
palibenso china.”

20 Koma Edomu anayankhanso kuti,

“Musadutse.”

Kenaka Edomu anatuluka ndi gulu lankhondo lalikulu komanso lam-
phamvu. 21 Edomu anakaniza Israeli kuti adutse m'dziko lake, choncho
Israeli anabwerera.

*Aaroni Amwalira*

22 Gulu lonse la Aisraeli linachoka ku Kadesi ndipo linafika ku phiri
la Hori. 23 Ali pa phiri la Hori, pafupi ndi malire a Edomu, Yehova
anati kwa Mose ndi Aaroni, 24 "Aaroni adzakakhala ndi anthu a mtundu
wake, sadzalowa m'dziko limene ndapereka kwa Aisraeli, chifukwa nonse
munandiwukira motsutsana ndi malamulo anga ku madzi a ku Meriba.
25 Tenga Aaroni ndi mwana wake wamwamuna Eliezara ndipo ukwere
nawo ku phiri la Hori. 26 Uvule Aaroni zovala zake ndipo umuveke mwana
wake Eliezara, pakuti Aaroni adzafera komweko, ndipo adzakakhala ndi
anthu a mtundu wake."

27 Mose anachita monga Yehova anamulamulira: Anapita ku phiri la
Hori gulu lonse likuona. 28 Pamenepo Mose anavula Aaroni zovala zake
ndi kuveka mwana wake Eliezara. Aaroni anafa kumeneko pamwamba
pa phirilo. Koma Mose ndi Eliezara anatsika ku phiriko, 29 ndipo pamene
anthu onse anamva kuti Aaroni wafa, nyumba yonse ya Israeli inamulira
Aaroniyo masiku makumi atatu.

# 21

*Kuwonongedwa kwa Aradi*

1 Mfumu ya Akanaani ya ku Aradi, imene inkakhala ku Negevi, itamva
kuti Aisraeli akubwera kudzera msewu wopita ku Atarimu, inachita
nkhondo ndi Aisraeli nigwira ena mwa iwo. 2 Ndipo Israeli anachita
lonjezo ili kwa Yehova: "Mukapereka anthu awa m'dzanja lathu ife
tidzawonongeratu mizinda yawo." 3 Yehova anamva pempho la Aisraeli
ndipo anapereka Akanaaniwo kwa iwo. Anawawononga pamodzi ndi
mizinda yawo. Kotero malowo anatchedwa Horima.

*Njoka Yamkuwa*

4 Aisraeli anayenda kuchokera ku phiri la Hori kudzera njira ya ku
Nyanja Yofiira kuzungulira dziko la Edomu. Koma anthu anataya mtima
m'njiramo 5 ndipo anayankhula motsutsana ndi Mulungu ndi Mose, nati,
"Chifukwa chiyani munatitulutsa kuchoka m'dziko la Igupto kuti tidzafere
m'chipululu muno? Kuno kulibe chakudya, kulibe madzi ndipo chakudya
cha chabechabechi tatopa nacho."

6 Choncho Yehova anatumiza njoka zaululu pakati pawo. Zinaluma
anthu ndipo Aisraeli ambiri anafa. 7 Anthuwo anabwera kwa Mose ndi
kunena kuti, "Tachimwa chifukwa tayankhula motsutsana ndi Yehova
komanso inu. Pempherani kwa Yehova kuti atichotsere njokazi." Tsono
Mose anapempherera anthuwo.

8 Yehova anati kwa Mose, "Upange njoka yaululu ndipo uyipachike pa
mtengo. Aliyense amene walumidwa akangoyang'ana njokayo adzakhala
ndi moyo." 9 Pamenepo Mose anapanga njoka yamkuwa ndi kuyipachika
pa mtengo. Ndipo aliyense wolumidwa akayang'ana njoka yamkuwayo
ankakhala ndi moyo.

*Ulendo wa ku Mowabu*

10 Aisraeli anayendabe nakamanga misasa yawo ku Oboti. 11 Kenaka
anasamuka ku Oboti nakamanga misasa yawo ku Iye-Abarimu,

m'chipululu chimene chili kummawa kwa Mowabu, kotulukira dzuwa.
12 Kuchoka kumeneko anayendabe nakamanga misasa yawo m'chigwa
cha Zeredi. 13 Anasamukanso kumeneko nakamanga moyandikana ndi
Arinoni m'dera limene lili m'chipululu chimene chimafika m'dziko la
Aamori. Arinoni ndiwo malire a Mowabu ndi Aamori. 14 N'chifukwa
chake Buku la Nkhondo za Yehova limati,
"Mzinda wa Wahebu uli mu Sufa,
mu zigwa za Arinoni, 15 ku matsitso a zigwa
amene afika mpaka ku Ari
nakhudza malire a dziko la Mowabu."
16 Kuchokera kumeneko anapitirira mpaka ku Beeri, pa chitsime chomwe
Yehova anawuza Mose kuti, "Sonkhanitsa anthu pamodzi ndipo ndidzawapatsa madzi."
17 Pamenepo Aisraeli anayimba nyimbo iyi:
"Tulutsa madzi, chitsime iwe!
Chiyimbireni nyimbo,
18 chitsime chomwe anakumba mafumu,
chomwe anakumba anthu omveka,
ndi ndodo zawo zaufumu ndi ndodo zawo zoyendera."
Kenaka anachoka ku chipululu ndi kupita ku Matana. 19 Kuchoka ku
Matana anapita ku Nahalieli, kuchoka ku Nahalieli anapita ku Bamoti,
20 ndipo atachoka ku Bamoti anapita ku chigwa cha dziko la Mowabu
kudzera njira ya pamwamba pa phiri la Pisiga, moyang'anana ndi
Yesimoni.

*Kugonjetsedwa kwa Sihoni ndi Ogi*

21 Aisraeli anatumiza amithenga kwa Sihoni mfumu ya Aamori, kuti,
22 "Tiloleni kuti tidutse m'dziko mwanu. Sitidzapatukira m'minda mwanu kapena mu mpesa wanu kapena kumwa madzi m'chitsime chili chonse. Tidzayenda mu msewu waukulu wa mfumu mpaka titadutsa malire a dziko lanu."
23 Koma Sihoni sanalole kuti Aisraeli adutse m'dziko mwake. Iye
anasonkhanitsa pamodzi ankhondo ake onse kuti akamenyane ndi Aisraeli
m'chipululu. Atafika pa Yahazi anamenyana ndi Aisraeli. 24 Koma
Aisraeli anamupha ndi kulanda dziko lake kuchokera ku Arinoni mpaka
ku Yaboki, kulekezera m'malire a dziko la Aamoni, chifukwa malire a
dziko la Aamoni anali otetezedwa. 25 Ndipo Aisraeli analanda mizinda
yonse ya Aamori, nakhalamo kuphatikizapo Hesiboni ndi midzi yake
yozungulira. 26 Hesiboni unali mzinda wa Sihoni mfumu ya Aamori,
yemwe anamenyana ndi mfumu yakale ya dziko la Mowabu. Lonselo
linakhala dziko lake mpaka ku Arinoni.
27 N'chifukwa chake alakatuli amati:
"Bwerani ku Hesiboni, mzindawo umangidwenso;
mzinda wa Sihoni ukhazikike.

28 "Moto unabuka ku Hesiboni,
malawi a moto kuchokera mu mzinda wa Sihoni.
Unanyeketsa Ari mzinda wa ku Mowabu,
nzika za ku malo okwera a Arinoni.
29 Tsoka kwa iwe Mowabu!
Mwawonongedwa inu anthu a ku Kemosi!
Ana ake aamuna wawasandutsa ngati anthu othawathawa
ndipo ana ake aakazi ngati akapolo,

akapolo a Sihoni, mfumu ya Aamori.

30 “Koma ife tawagonjetsa;
Hesiboni wawonongedwa m’njira monse mpaka kufika ku Diboni.
Tawaphwasula mpaka ku mzinda wa Nofa,
mzinda womwe umafika ku Medeba.
31 “Choncho Aisraeli anakhala m’dziko la Aamori.”
32 Mose atatumiza azondi ku Yazeri, Aisraeliwo analanda midzi yozun-
gulira ndi kuthamangitsa Aamori omwe ankakhala kumeneko. 33 Kenaka
anabwerera, nadzera njira ya ku Basani. Choncho Ogi mfumu ya ku
Basani ndi gulu lake lonse lankhondo anatuluka kukakumana nawo ndipo
anamenyana nawo ku Ederi.
34 Yehova anati kwa Mose, “Usachite naye mantha pakuti ndamupereka
m’manja mwako pamodzi ndi gulu lake lonse lankhondo ndi dziko lake
lomwe. Ndipo uchite kwa iye zimene unachita Sihoni mfumu ya Aamori,
amene ankalamulira ku Hesiboni.”
35 Choncho Aisraeli anapha Ogi pamodzi ndi ana ake aamuna ndi
gulu lake lonse la nkhondo. Palibe ndi mmodzi yemwe amene anatsala
wamoyo, ndipo analanda dziko lakelo.

# 22

*Balaki Ayitana Balaamu*

1 Aisraeli anayenda kupita ku zigwa za Mowabu nakamanga misasa
yawo tsidya lina la Yorodani moyang’anana ndi Yeriko.
2 Tsono Balaki mwana wa Zipori anaona zonse zimene Aisraeli anachi-
tira Aamori, 3 ndipo Amowabu anaopa anthuwo chifukwa analipo ambiri.
Amowabuwo anachita mantha kwambiri mpaka ananjenjemera chifukwa
cha Aisraeli.
4 Iwo anati kwa akuluakulu a ku Midiyani, “Gulu ili lidzabudula zonse
zimene zatizungulira monga momwe ng’ombe yothena imathera udzu wa
ku tchire.”
Tsono Balaki mwana wa Zipori, yemwe anali mfumu ya Mowabu
pa nthawi imeneyo, 5 anatumiza amithenga kwa Balaamu mwana wa
Beori, yemwe anali ku Petori, pafupi ndi mtsinje, m’dziko la kwawo kuti
akamuyitane. Balaki anati:
“Taonani, anthu ochokera ku Igupto abwera, adzaza dziko lonse
ndipo akufuna kuchita nane nkhondo. 6 Tsopano bwera, utemberere
anthu amenewa chifukwa ndi amphamvu kwambiri kuposa ine. Mwina
ndingadzawagonjetse ndi kuwatulutsira kunja kwa dzikoli chifukwa
ndikudziwa kuti amene umawadalitsa amadalitsika, ndipo amene
umawatemberera amatembereredwa.”
7 Akuluakulu a Mowabu ndi akuluakulu a Midiyani ananyamuka
atatenga ndalama zokalipirira mawula. Atafika kwa Balaamu, ana-
muwuza zomwe Balaki ananena.
8 Balaamu anawawuza kuti, “Mugone konkuno usiku uno, ndipo
ndikuyankhani zomwe Yehova andiwuze.” Choncho akuluakulu a
Amowabu anagona kwa Balaamu.
9 Mulungu anabwera kwa Balaamu namufunsa kuti, “Kodi anthu ali ndi
iwewa ndani?”
10 Balaamu anayankha Mulungu kuti, “Balaki mwana wa Zipori, mfumu
ya Mowabu, ananditumizira uthenga uwu: 11 ‘Taonani, anthu amene

achokera ku dziko la Igupto adzaza dziko lonse. Tsopano bwera
udzawatemberere m'malo mwanga. Mwina ndidzatha kumenyana nawo
ndi kuwatulutsa.' "
12 Koma Mulungu anawuza Balaamu kuti, "Usapite nawo. Usawatem-
berere anthu amenewo chifukwa ndi odalitsika."
13 Mmawa mwake Balaamu anadzuka ndi kuwuza akuluakulu a Balaki
aja kuti, "Bwererani ku dziko la kwanu chifukwa Yehova sanandilole kuti
ndipite nanu."
14 Kotero akuluakulu a Mowabu anabwerera kwa Balaki ndi kukanena
kuti, "Balaamu wakana kubwera nafe."
15 Kenaka Balaki anatumanso akuluakulu ena ambiri ndi olemekezeka
kwambiri kuposa oyamba aja ndipo 16 anafika kwa Balaamu nati;

"Zomwe Balaki mwana wa Zipori akunena ndi izi: 'Usalole kuti
china chilichonse chikulepheretse kubwera kwa ine, 17 chifukwa ndidza-
kulipira bwino kwambiri ndipo ndidzakuchitira chilichonse chimene
unganene. Bwera ndipo uwatemberere anthu amenewa m'malo
mwanga.' "

18 Koma Balaamu anayankha atumiki a Balaki kuti, "Ngakhale Balaki
atandipatsa nyumba yaufumu yodzaza ndi siliva ndi golide sindingachite
chilichonse chachikulu kapena chaching'ono kuposa kuchita lamulo la
Yehova Mulungu wanga. 19 Tsopano mukhale kuno usiku uno monga ena
anachitira, ndidzaona chimene Yehova adzandiwuza."
20 Usiku umenewo Mulungu anabwera kwa Balaamu ndipo anati,
"Popeza anthu awa abwera kudzakuyitana, nyamuka, pita nawo koma
ukachite zokhazo zimene ndikuwuze."

### *Bulu Ayankhula*

21 Balaamu anadzuka mmawa, namanga bulu wake wamkazi ndipo
anapita ndi akuluakulu a Mowabu. 22 Koma Mulungu anakwiya kwambiri
pamene ankapita ndipo mngelo wa Yehova anayima pa njira kutsutsana
naye. Balaamu anakwera bulu wake wamkazi ndipo antchito ake awiri
anali naye. 23 Pamene buluyo anaona mngelo wa Yehova atayima pa njira
ndi lupanga m'manja mwake, anapatukira kumbali kwa msewu napita
kutchire. Balaamu anamumenya kuti abwerere mu msewu.
24 Kenaka mngelo wa Yehova anayima m'kanjira kakang'ono pakati
pa minda iwiri ya mpesa yokhala ndi makoma mbali zonse 25 Bulu uja
ataona mngelo wa Yehova anadzipanikiza ku khoma, kukhukhuza phazi
la Balaamu kukhomako. Ndipo pomwepo Balaamu anamenya buluyo
kachiwiri.
26 Kenaka mngelo wa Yehova anapita patsogolo ndi kuyima pamalo
opanikizika pomwe panalibe poti n'kutembenukira ku dzanja lamanja
kapena lamanzere. 27 Buluyo ataonanso mngelo wa Yehova uja, anagona
pansi Balaamu ali pa msana, ndipo iye anakwiya ndi kumumenya ndi
ndodo yake. 28 Pamenepo Yehova anayankhulitsa bulu uja, ndipo buluyo
anati kwa Balaamu, "Ndakuchitirani chiyani kuti mundimenye katatuka?"
29 Balaamu anati kwa buluyo, "Wandipusitsa, ndikanakhala ndi lupanga
m'manja mwanga, ndikanakupha pomwe pano."
30 Buluyo anati kwa Balaamu, "Kodi sindine bulu wanu, amene mumak-
wera nthawi zonse kufikira lero? Kodi ndinakuchitiranipo zoterezi?"
Iye anati "Ayi."
31 Pomwepo Yehova anatsekula maso Balaamu ndipo anaona mngelo
wa Yehovayo ali chiyimire pa njira ndi lupanga losolola. Tsono iye
anawerama nalambira pamaso pake.

32 Mngelo wa Yehova anamufunsa kuti, “Chifukwa chiyani wamenya
bulu wako katatu? Taona, Ine ndabwera kudzakutsutsa chifukwa ulendo
wakowu ndi woyipa pamaso panga. 33 Buluyu anandiona ndi kupatuka
katatu aka. Akanakhala kuti sanapatuke, ndikanakupha tsopano, koma
buluyu n’kanamusiya ndi moyo.”
34 Balaamu anati kwa mngelo wa Yehova uja, “Ndachimwa. Sin-
dinadziwe kuti munayima pa njira kunditsutsa. Tsopano ngati Inu
simunakondwe, ineyo ndibwerera.”
35 Mngelo wa Yehova anati kwa Balaamu, “Pita ndi anthuwa koma
ukayankhule zokhazo zimene ndikakuwuze.” Choncho Balaamu anapita
ndi akuluakulu a Balaki.
36 Balaki atamva kuti Balaamu akubwera, anapita kukakumana naye
ku mzinda wa Mowabu umene unali m’malire a Arinoni, m’mphepete
mwa dziko lake. 37 Balaki anati kwa Balaamu, “Kodi sindinakutumizire
uthenga woti ubwere msanga? Chifukwa chiyani sunabwere kwa ine?
Kodi sindingathe kukulipira mokwanira?”
38 Balaamu anayankha Balaki kuti, “Taonani, ndabwera kwa inu lero,
kodi ine ndili ndi mphamvu zoti n’kuyankhula chilichonse? Inetu
ndiyenera kuyankhula zokhazo zimene Mulungu wandiwuza.”
39 Pamenepo Balaamu anapita pamodzi ndi Balaki ku Kiriati-Huzoti.
40 Balaki anapereka nsembe ng’ombe ndi nkhosa, ndipo anapereka
zina kwa Balaamu ndi kwa akuluakulu omwe anali naye. 41 Mmawa
mwake Balaki anatenga Balaamu napita limodzi ku Bamoti Baala, ndipo
kumeneko anakaonako gulu lina la Aisraeliwo.

# 23

*Uthenga Woyamba wa Balaamu*

1 Balaamu anati kwa Balaki, “Mundimangire maguwa ansembe asanu
ndi awiri pano, ndipo mukonzenso ng’ombe zazimuna zisanu ndi ziwiri
ndi nkhosa zazimuna zisanu ndi ziwiri.” 2 Balaki anachita monga
Balaamu ananenera ndipo awiriwo anapereka ng’ombe imodzi ndi nkhosa
yayimuna imodzi pa guwa lansembe lililonse.
3 Kenaka Balaamu anati kwa Balaki, “Khalani pano pafupi ndi nsembe
yanu ineyo ndipite pambali. Mwina Yehova adzabwera kuti akumane
nane. Chilichonse chimene akandionetse ndidzakuwuzani” Choncho
anapita ku malo okwera a chipululu.
4 Mulungu anakumana naye ndipo Balaamu anati, “Ndakonza maguwa
asanu ndi awiri ndipo pa guwa lililonse ndaperekapo nsembe ya ng’ombe
yayimuna imodzi ndi nkhosa yayimuna imodzinso.”
5 Yehova anawuza Balaamu kuti, “Bwerera kwa Balaki ndipo uka-
muwuze uthenga uwu.”
6 Ndipo anabwerera kwa iye namupeza atayima pafupi ndi nsembe
yake pamodzi ndi akuluakulu onse a Mowabu. 7 Ndipo Balaamu ananena
uthenga wake:
“Balaki ananditenga kuchoka ku Aramu,
 mfumu ya ku Mowabu kuchokera ku mapiri a kummawa.
Iye anati, ‘Bwera, temberera Yakobo m’malo mwanga,
 pita nyoza Israeli.’
8 Ndingatemberere bwanji
 amene Mulungu sanawatemberere?
Ndinganyoze bwanji
 amene Yehova sanawanyoze?

9 Kuchokera pamwamba pa mapiri ndikuona anthu,
ndikuwaona kuchokera pa zitunda.
Ndikuona anthu okhala pawokha,
osakhala m'gulu limodzi ndi mitundu ina.
10 Ndani angawerenge zidzukulu za Yakobo zochuluka ngati fumbi,
kapena chimodzi mwa zigawo zinayi za Israeli?
Lekeni ndife imfa ya oyera mtima,
ndi chimaliziro changa chikhale ngati chawo!"
11 Balaki anati kwa Balaamu, "Wandichitira chiyani? Ndinakuyitana
kuti utemberere adani anga, ndipo taona, sunachite chilichonse koma
kuwadalitsa!"
12 Iye anayankha kuti, "Kodi sindinayenera kuyankhula zimene Yehova
anandiwuza?"

### *Uthenga Wachiwiri wa Balaamu*

13 Kenaka Balaki anawuza Balaamu kuti, "Tiye tipite limodzi ku malo
ena komwe ungawaone. Udzangoona gulu limodzi osati onsewo. Ndipo
pamenepo, ukawatemberere m'malo mwanga."
14 Tsono anamutengera
ku munda wa Zofimu pamwamba pa phiri la Pisiga ndipo kumeneko
anamanga maguwa ansembe asanu ndi awiri ndipo anapereka nsembe
ng'ombe yayimuna imodzi ndi nkhosa yayimuna imodzi pa guwa
lansembe lililonse.
15 Balaamu anawuza Balaki kuti, "Khalani pano pafupi ndi nsembe yanu
pamene ine ndikukakumana ndi Mulungu cha uko."
16 Yehova anakumana ndi Balaamu ndipo anamuyankhula kuti, "Bwer-
era kwa Balaki ndipo ukamuwuze uthenga uwu."
17 Ndipo anapita kwa iye ndipo anamupeza atayimirira pafupi ndi
nsembe yake pamodzi ndi akuluakulu a ku Mowabu. Balaki anafunsa
Balaamu kuti, "Yehova wayankhula chiyani?"
18 Pamenepo Balaamu ananena uthenga wake:
"Nyamuka Balaki ndipo tamvera;
Undimvere iwe mwana wa Zipori.
19 Mulungu si munthu kuti aname,
kapena mwana wa munthu kuti asinthe maganizo ake.
Kodi amayankhula koma osachita?
Kodi amalonjeza koma osakwaniritsa?
20 Wandilamula kuti ndidalitse,
Iyeyo wadalitsa ndipo sindingasinthe.

21 "Palibe kuwukira kulikonse kumene wakuona mwa Yakobo,
sanaone chovuta mu Israeli.
Yehova Mulungu wawo ali nawo:
mfuwu wa mfumu uli pakati pawo.
22 Mulungu wowatulutsa m'dziko la Igupto,
ali ndi mphamvu ngati za njati.
23 Palibe matsenga amene angalimbane ndi Yakobo,
palibe mawula amene angalimbane ndi Israeli.
Tsopano za Yakobo ndi Israeli adzanena kuti,
'Onani zimene Mulungu wachita!'
24 Taonani, anthu anyamuka ngati mkango waukazi;
adzuka okha ngati mkango waumuna
umene supuma mpaka utadya nyama imene wagwira
ndi kumwa magazi a nyama yogwidwayo."

25 Ndipo Balaki anati kwa Balaamu, “Usawatemberere ndi pang’ono
pomwe kapena kuwadalitsa!
26 “Balaamu anayankha Balaki kuti, ‘Kodi sindinakuwuzeni kuti ndiyen-
era kuchita zimene Yehova wanena?’ ”

*Uthenga Wachitatu wa Balaamu*

27 Kenaka Balaki anati kwa Balaamu, “Bwera ndikutengere ku malo ena.
Mwina chidzamukondweretsa Mulungu kuti uwatemberere kumeneko
m’malo mwanga.” 28 Ndipo Balaki anamutengera Balaamu pamwamba
pa Peori, poyang’anana ndi chipululu.
29 Balaamu anati kwa Balaki, “Mundimangire maguwa ansembe asanu
ndi awiri pano ndipo mundikonzere ng’ombe zazimuna zisanu ndi
ziwiri, nkhosa zazimuna zisanu ndi ziwiri.” 30 Balaki anachita monga
Balaamu ananenera ndipo anapereka nsembe ng’ombe imodzi yayimuna
ndi nkhosa imodzi yayimuna pa guwa lililonse.

# 24

1 Tsopano Balaamu ataona kuti kunakomera Yehova kudalitsa Israeli,
sanapitenso ku mawula monga ankachitira kale, koma kuyang’ana ku
chipululu. 2 Balaamu atayang’ana, anaona Aisraeli atamanga misasa yawo
fuko ndi fuko. Pamenepo mzimu wa Mulungu unabwera pa iye 3 ndipo
ananena uthenga wake:

“Uthenga wa Balaamu mwana wa Beori,
uthenga wa amene diso lake ndi lotsekuka,
4 uthenga wa amene amamva mawu a Mulungu,
yemwe amaona masomphenya wochokera kwa Wamphamvuzonse,
yemwe amagwa chafufumimba, koma maso ake ali chipenyere:

5 “Matenti ako ndi okongola kwambiri iwe Yakobo,
misasa yako, iwe Israeli!

6 “Monga zigwa zotambalala,
monga minda m’mbali mwa mtsinje,
monga aloe wodzalidwa ndi Yehova,
monga mikungudza m’mbali mwa madzi.
7 Madzi adzayenderera m’mitsuko yake;
mbewu zake zidzakhala ndi madzi ambiri.

“Mfumu yake idzakhala yamphamvu kuposa Agagi;
ufumu wake udzakwezedwa.

8 “Mulungu womutulutsa m’dziko la Igupto
ali ndi mphamvu ngati za njati.
Amawononga mitundu yomuwukira
ndi kuphwanya mafupa awo,
amalasa ndi mivi yake.
9 Monga mkango waumuna, amabisala nagona pansi,
monga mkango waukazi, adzamuputa ndani?

“Amene adalitsa iwe, adalitsike
ndipo amene atemberera iwe, atembereredwe!”
10 Kenaka Balaki anakwiyira Balaamu. Anawomba m’manja ndi kunena
naye kuti, “Ndinakuyitana kuti utemberere adani anga, koma taona,

wawadalitsa katatu konseka. 11 Tsopano choka msanga uzipita kwanu!
Ndinanena kuti ndidzakulipira bwino kwambiri, koma Yehova sanafune
kuti ulandire malipirowo."

12 Balaamu anayankha Balaki kuti, "Kodi sindinawawuze amithenga
amene munawatumiza kwa ine, 13 kuti ngakhale Balaki atandipatsa
nyumba yake yaufumu yodzaza ndi siliva ndi golide sindingathe kuchita
zinthu mwa ine ndekha, zabwino kapena zoyipa, kuposa lamulo la Yehova
ndi kuti ndiyenera kunena zokhazo zimene Yehova akunena? 14 Tsopano
ndikupita kwa anthu anga, koma tabwerani ndikuchenjezeni zimene
anthu awa adzachitira anthu anu masiku akubwerawa."

### *Uthenga Wachinayi wa Balaamu*

15 Ndipo iye ananena uthenga wake nati,
"Uthenga wa Balaamu mwana wa Beori,
uthenga wa amene diso lake ndi lotsekuka.
16 Uthenga wa amene amamva mawu a Mulungu,
amene ali ndi nzeru zochokera kwa Wammwambamwamba,
amene amaona masomphenya wochokera kwa Wamphamvuzonse,
amene amagwa chafufumimba koma diso lake lili lotsekuka:

17 "Ndikumuona iye koma osati tsopano;
ndikumupenya iye koma osati pafupi.
Nyenyezi idzatuluka mwa Yakobo;
ndodo yaufumu idzatuluka mwa Israeli.
Iye adzagonjetsa Mowabu
ndi kugonjetsa ana onse a Seti.
18 Edomu adzagonjetsedwa;
Seiri, mdani wake, adzawonongedwa
koma mphamvu za Israeli zidzachuluka.
19 Wolamulira adzachokera mwa Yakobo
ndipo adzawononga otsala a mu mzindamo."

### *Uthenga Wachisanu wa Balaamu*

20 Kenaka Balaamu anaona Aamaleki ndipo ananena uthenga wake uwu:
"Aamaleki anali oyamba mwa mitundu ya anthu
koma potsiriza pake adzawonongeka."

### *Uthenga Wachisanu ndi Chimodzi wa Balaamu*

21 Kenaka anaonanso Akeni ndipo ananena uthenga wake,
"Malo amene mukukhalamo ndi otetezedwa,
chisa chanu chinayikidwa pa thanthwe;
22 komabe inu Akeni mudzawonongedwa,
pamene Asuri adzakutengeni ukapolo."

### *Uthenga Wachisanu ndi Chiwiri wa Balaamu*

23 Ndipo ananenanso uthenga wina kuti,
"Aa, ndani adzakhala ndi moyo Mulungu akachita zimenezi?
24 Sitima zapamadzi zidzabwera kuchokera ku madooko a Kitimu;
kupondereza Asuri ndi Eberi,
koma iwonso adzawonongeka."

25 Pamenepo Balaamu ananyamuka ndi kubwerera kwawo ndipo Balaki
anapitanso njira yake.

# 25

*Aisraeli Achita Chigololo*

1 Aisraeli akukhala ku Sitimu, anayamba kuchita chigololo ndi akazi
a ku Mowabu, 2 amene ankawayitana ku nsembe za milungu yawo.
Anthuwo anadya chakudya chopereka kwa milungu ndi kupembedza
milunguyo. 3 Motero Aisraeli anapembedza nawo Baala-Peori ndipo
Yehova anawapsera mtima kwambiri.

4 Pamenepo Yehova anawuza Mose kuti, “Tenga atsogoleri onse a anthu
awa, uwaphe poyera, pamaso pa Yehova kuti mkwiyo waukulu wa Yehova
uchoke pa Israeli.”

5 Choncho Mose anawuza oweruza a Israeli kuti, “Aliyense wa inu
ayenera kupha anthu ake amene anapembedza nawo Baala-Peori.”

6 Kenaka mwamuna wina wa ku Israeli anabweretsa ku banja lake
mkazi wa Chimidiyani pamaso pa Mose ndi anthu onse a Israeli pamene
ankalira pa khomo la tenti ya msonkhano. 7 Finehasi mwana wa Eliezara,
mwana wa wansembe Aaroni ataona izi, anachoka pa msonkhanowo,
natenga mkondo m’dzanja lake. 8 Ndipo anatsatira Mwisraeliyu mpaka
m’tenti yake. Anasolola mkondowo ndi kubaya awiriwo kupyola Mwis-
raeliyo mpaka m’thupi la mkaziyo. Pamenepo mliri unaleka pakati pa
Aisraeli. 9 Pa mliriwo, anthu okwana 24,000 anafa.
10 Yehova anawuza Mose kuti, 11 “Finehasi mwana wa Eliezara,
mwana wa wansembe Aaroni wabweza mkwiyo wanga pa Aisraeli
chifukwa sanalole kuti wina aliyense apembedze mulungu wina koma
Ine ndekha. N’chifukwa chake sindinawawononge mu mkwiyo wanga.
12 Tsono muwuze kuti ndikhazikitsa pangano langa la mtendere ndi iye.
13 Ndikupangana naye pangano la unsembe wosatha, iyeyo pamodzi ndi
zidzukulu zake zonse, chifukwa sanalole kuti anthu awukire Ine Mulungu,
ndipo anachita ntchito yopepesera machimo Aisraeli.”

14 Dzina la Mwisraeli yemwe anaphedwa ndi mkazi wa Chimidiyani
anali Zimuri mwana wa Salu, mtsogoleri wa banja la Simeoni. 15 Ndipo
dzina la mkazi wa Chimidiyani, yemwe anaphedwayo, linali Kozibi
mwana wa Zuri, mtsogoleri wa fuko la ku Midiyaniko.

16 Yehova anawuza Mose kuti, 17 “Amidiyani ndi adani anu ndipo
uwaphe, 18 chifukwa ankakuonani inu ngati adani awo pamene anaku-
pusitsani pa nkhani ya ku Peori, ndiponso za mlongo wawo Kozibi, mwana
wamkazi wa mtsogoleri wa Amidiyani, mkazi yemwe anaphedwa pamene
mliri unabwera chifukwa cha zimene zinachitika ku Peori.”

# 26

*Kalembera Wachiwiri*

1 Utatha mliri Yehova anati kwa Mose ndi Eliezara mwana wa Aaroni,
2 “Werengani Aisraeli onse mwa mabanja awo, onse a zaka makumi awiri
kapena kuposera pamenepo omwe angathe kugwira ntchito ya usilikali
m’gulu lankhondo la Israeli.” 3 Kotero mu zigwa za Mowabu pafupi ndi
mtsinje wa Yorodani ku Yeriko, Mose ndi wansembe Eliezara anayankhula
nawo kuti, 4 “Werengani amuna a zaka makumi awiri kapena kuposera
pamenepo, monga momwe Yehova walamulira Mose.”

Aisraeli omwe anachokera ku Igupto ndi awa:

5 Zidzukulu za Rubeni, mwana woyamba wamwamuna wa Israeli, zinali izi:
kuchokera mwa Hanoki, fuko la Ahanoki;
kuchokera mwa Palu, fuko la Apalu;
6 kuchokera mwa Hezironi, fuko la Ahezironi;
kuchokera mwa Karimi, fuko la Akarimi.
7 Awa anali mafuko a Rubeni: onse amene anawerengedwa analipo 43,730.
8 Mwana wa Palu anali Eliabu, 9 ndipo ana a Eliabu anali Nemueli,
Datani ndi Abiramu. Datani ndi Abiramu anali gulu la akuluakulu aja
amene anawukira Mose ndi Aaroni ndipo analinso m'gulu la otsatira
Kora pamene anawukira Yehova. 10 Nthaka inang'ambika ndi kuwameza
pamodzi ndi Kora, kotero kuti gulu lawo linafa pamene moto unapsereza
anthu 250 aja, nasanduka chenjezo. 11 Koma ana a Kora sanafe nawo.

12 Zidzukulu za Simeoni mwa mafuko awo zinali izi:
kuchokera mwa Nemueli, fuko la Anemuele;
kuchokera mwa Yamini, fuko la Ayamini;
kuchokera mwa Yakini fuko la Ayakini;
13 kuchokera mwa Zera, mbumba ya Zera;
kuchokera mwa Sauli, fuko la Asauli.
14 Awa anali mafuko a Simeoni. Iwowa analipo amuna 22,200.

15 Zidzukulu za Gadi mwa mafuko awo ndi izi:
kuchokera mwa Zefoni, fuko la Azefoni;
kuchokera mwa Hagi, fuko la Ahagi;
kuchokera mwa Suni, fuko la Asuni;
16 kuchokera mwa Ozini, fuko la Aozini;
kuchokera mwa Eri, fuko la Aeri;
17 kuchokera mwa Arodi, fuko la Aarodi;
kuchokera mwa Arieli, fuko la a Areli.
18 Awa ndiwo anali mafuko a Gadi. Onse amene anawerengedwa analipo 40,500.

19 Eri ndi Onani anali ana aamuna a Yuda, koma anafera mu Kanaani.
20 Zidzukulu za Yuda monga mwa mafuko awo zinali izi:
kuchokera mwa Sela, fuko la Asera;
kuchokera mwa Perezi, fuko la Aperezi;
kuchokera mwa Zera, mbumba ya Zera.
21 Zidzukulu za Perezi zinali izi:
kuchokera mwa Hezironi, fuko la Ahezironi;
kuchokera mwa Hamuli, fuko la Ahamuli.
22 Awa ndiwo anali mafuko a Yuda. Amene anawerenga analipo 76,500.

23 Zidzukulu za Isakara monga mwa mafuko awo zinali izi:
kuchokera mwa Tola, fuko la Atola;
kuchokera mwa Puwa, fuko la Apuwa;
24 kuchokera mwa Yasubu, fuko la Ayasubu.
Kuchokera mwa Simironi, fuko la Asimironi.
25 Awa ndi amene anali a fuko la Isakara. Amene anawerengedwa analipo 64,300.

26 Zidzukulu za Zebuloni mwa mafuko awo zinali izi:

kuchokera mwa Seredi, fuko la Aseredi;
kuchokera mwa Eloni, fuko la Aeloni;
kuchokera mwa Yahaleeli, fuko la Ayahaleeli.
27 Awa ndiwo anali mafuko a Zebuloni. Amene anawerengedwa analipo 60,500.

28 Zidzukulu za Yosefe mwa mafuko awo kupyolera mwa Manase ndi Efereimu zinali izi:
29 Zidzukulu za Manase:
kuchokera mwa Makiri, fuko la Amakiri (Makiri anali abambo ake a Giliyadi);
kuchokera mwa Giliyadi, fuko la Agiliyadi.
30 Izi ndizo zinali zidzukulu za Giliyadi;
kuchokera mwa Iyezeri, fuko la Aiyezeri;
kuchokera mwa Heleki, fuko la Aheleki;
31 kuchokera mwa Asirieli, fuko la Aasirieli;
kuchokera mwa Sekemu, fuko la Asekemu;
32 kuchokera mwa Semida, fuko la Asemida;
kuchokera mwa Heferi, fuko la Aheferi.
33 (Zelofehadi mwana wa Heferi analibe ana aamuna koma ana aakazi okha, amene mayina awo anali: Mala, Nowa, Hogila, Milika ndi Tiriza.)
34 Awa ndiwo anali mafuko a Manase. Amene anawerengedwa analipo 52,700.
35 Zidzukulu za Efereimu monga mwa mafuko awo zinali izi;
kuchokera mwa Sutela, fuko la Asutela;
kuchokera mwa Bekeri, fuko la Abekeri;
kuchokera mwa Tahani, fuko la Atahani.
36 Zidzukulu za Sutela zinali izi:
kuchokera mwa Erani, fuko la Aerani.
37 Awa ndiwo anali mafuko a Efereimu. Amene anawerengedwa analipo 32,500.
Zimenezi zinali zidzukulu za Yosefe monga mwa mafuko awo.

38 Zidzukulu za Benjamini monga mwa mabanja awo zinali izi:
kuchokera mwa Bela, fuko la Abela;
kuchokera mwa Asibeli, fuko la Aasibeli;
kuchokera mwa Ahiramu, fuko la Ahiramu;
39 kuchokera mwa Sufamu, fuko la Asufamu;
kuchokera mwa Hufamu, fuko la Ahufamu;
40 Zidzukulu za Bela kupyolera mwa Aridi ndi Naamani zinali izi:
kuchokera mwa Aridi, fuko la Aaridi;
kuchokera mwa Naamani, fuko la Anaamani;
41 Awa ndiwo anali mabanja a Benjamini. Amene nawerengedwa analipo 45,600.

42 Zidzukulu za Dani mwa mabanja awo zinali izi:
kuchokera mwa Suhamu fuko la Asuhamu.
Izi zinali zidzukulu za Dani. 43 Onse a fuko la Asuhamu amene
anawerengedwa analipo 64,400.

44 Zidzukulu za Aseri monga mwa mafuko awo zinali izi:
kuchokera mwa Imina, fuko la Aimuna;

kuchokera mwa Isivi, fuko la Ayisivi;
kuchokera mwa Beriya, fuko la Aberiya;
45 ndipo kupyolera mwa zidzukulu za Beriya:
kuchokera mwa Heberi, fuko la Aheberi;
kuchokera mwa Malikieli, fuko la Amalikieli;
46 (Aseri anali ndi mwana wamkazi dzina lake Sera)
47 Awa ndiwo anali mafuko a Aseri. Onse amene anawerengedwa analipo 53,400.

48 Zidzukulu za Nafutali mwa mafuko awo zinali izi:
kuchokera mwa Yahazeeli, fuko la Ayahazeeli;
kuchokera mwa Guni, fuko la Aguni;
49 kuchokera mwa Yezeri, fuko la Ayezeri;
kuchokera mwa Silemu, fuko la Asilemu.
50 Awa ndiwo anali mafuko a Nafutali. Onse amene anawerengedwa analipo 45,400.

51 Chiwerengero chonse cha amuna mu Israeli chinalipo 601,730.

52 Yehova anawuza Mose kuti, 53 "Uwagawire dziko anthu awa kuti
likhale cholowa chawo molingana ndi chiwerengero cha mayina awo.
54 Gulu lalikulu ulipatse cholowa chachikulu, ndipo lochepa cholowa
chocheperapo. Gulu lililonse lilandire cholowa chake molingana ndi
chiwerengero cha amene anawerengedwa. 55 Dzikolo uligawe pochita
maere. Alandire cholowa chawocho potsata mayina a mafuko a makolo
awo. 56 Cholowa chawo uchigawe pakati pa fuko lalikulu ndi laling'ono
mwa maere."

57 Alevi omwe anawerengedwa monga mwa mafuko awo ndi awa:
kuchokera mwa Geresoni, fuko la Ageresoni;
kuchokera mwa Kohati, fuko la Akohati;
kuchokera mwa Merari, fuko la Amerari.
58 Awanso anali mabanja a Alevi:
banja la Alibini,
banja la Ahebroni,
banja la Amali,
banja la Amusi, fuko la Kora
banja la Akohati,
(Kohati anali abambo a Amramu. 59 Dzina la mkazi wa Amramu
linali Yokobedi, mdzukulu wa Levi, yemwe anabadwa mwa
Alevi mu Igupto. Yokobedi anaberekera Amramu Aaroni, Mose
ndi Miriamu mlongo wawo. 60 Aaroni anali abambo a Nadabu,
Abihu, Eliezara ndi Itamara. 61 Koma Nadabu ndi Abihu
anafa pamene anapereka nsembe pamaso pa Yehova ndi moto
wachilendo).

62 Alevi onse aamuna a mwezi umodzi kapena kuposera pamenepa analipo 23,000. Iwowo sanawerengedwe pamodzi ndi Aisraeli ena chifukwa sanalandire cholowa pakati pawo.

63 Awa ndi amene anawerengedwa ndi Mose ndi Eliezara wansembe
pamene ankawerenga Aisraeli pa zigwa za ku Mowabu m'mbali mwa

Yorodani ku Yeriko. [64] Mwa anthu amenewa panalibe ndi mmodzi
yemwe amene anali m'gulu la Aisraeli omwe Mose ndi wansembe Aaroni
anawawerenga m'chipululu cha Sinai; [65] Chifukwa Yehova anali atawuza
Aisraeliwo kuti adzafera ndithu m'chipululu, ndipo palibe ndi mmodzi
yemwe amene anatsala kupatula Kalebe mwana wa Yefune ndi Yoswa
mwana wa Nuni.

# 27

### *Ana Aakazi a Zelofehadi*

[1] Kenaka ana aakazi a Zelofehadi mwana wa Heferi, mwana wa Giliyadi,
mwana wa Makiri, mwana wamwamuna wa Manase, a m'mabanja a
Manase, mwana wa Yosefe anabwera. Mayina a ana aakaziwo anali
awa: Mala, Nowa, Hogila, Milika ndi Tiriza. Iwo anakayima [2] pa chipata
cha tenti ya msonkhano pamaso pa Mose, wansembe Eliezara, atsogoleri
ndi anthu onse, ndipo anati, [3] "Abambo athu anafera m'chipululu koma
sanali nawo m'gulu la anthu otsatira Kora, omwe anasonkhana pamodzi
kutsutsana ndi Yehova. Abambo athuwo anafa chifukwa cha tchimo lawo
ndipo sanasiye ana aamuna. [4] N'chifukwa chiyani dzina la abambo athu
lasowa pakati pa fuko lawo, kodi popeza analibe mwana wamwamuna?
Tipatseni cholowa chathu pakati pa abale a abambo athu."

[5] Tsono Mose anabweretsa nkhani yawo pamaso pa Yehova [6] ndipo
Yehova anati kwa iye, [7] "Zimene ana aakazi a Zelofehadi akunena ndi
zoona. Uyenera kuwapatsadi cholowa chawo pakati pa abale a abambo
awo ndipo uwapatse cholowa cha abambo awowo.

[8] "Uza Aisraeli kuti, 'Ngati munthu afa wosasiya mwana wamwamuna,
muzipereka cholowa chake kwa mwana wake wamkazi. [9] Ngati alibe
mwana wamkazi, muzipereka cholowa chakecho kwa abale ake. [10] Ngati
alibe abale muzipereka cholowa chake kwa abale a abambo ake. [11] Ngati
abambo ake analibe m'bale, muzipereka cholowa chakecho kwa mnansi
wake wa m'banja lake kuti chikhale chake. Ili likhale lamulo kwa Aisraeli,
monga momwe Yehova analamulira Mose.' "

### *Yoswa Alowa M'malo mwa Mose*

[12] Kenaka Yehova anati kwa Mose, "Kwera phiri la Abarimu kuti ukaone
dziko limene ndalipereka kwa Aisraeli. [13] Ukakaliona udzamwalira
ngati Aaroni m'bale wako, [14] chifukwa pamene anthu anawukira ku
madzi a Meriba m'chipululu cha Zini, inu nonse simunamvere lamulo
londilemekeza Ine ngati Woyera pamaso pawo." (Awa anali madzi a ku
Meriba ku Kadesi m'chipululu cha Zini).

[15] Mose anati kwa Yehova, [16] "Ngati n'kotheka Yehova, Mulungu wa
mizimu ya anthu onse, sankhani munthu woti ayang'anire gulu ili kuti
[17] alitsogolere potuluka ndi polowa, kuti anthu a Yehova asakhale ngati
nkhosa zopanda m'busa."

[18] Pamenepo Yehova anawuza Mose kuti, "Tenga Yoswa mwana wa
Nuni, munthu amene ali ndi mzimu wa utsogoleri, ndipo umusanjike
dzanja lako. [19] Umuyimiritse pamaso pa wansembe Eliezara ndi pamaso
pa gulu lonse ndipo umupatse mphamvu zolamulira, anthuwo akuona.
[20] Umupatse gawo lina la ulemerero wako kuti Aisraeli onse azimumvera.
[21] Ayime pamaso pa wansembe Eliezara, amene adzamudziwitse zimene
Yehova akufuna pogwiritsa ntchito Urimu. Iye akalamula, Aisraeli onse
azituluka ndipo akalamulanso, Aisraeliwo azibwereranso."

[22] Mose anachita monga Yehova anamulamulira. Anatenga Yoswa ndi
kumuyimiritsa pamaso pa Eliezara wansembe ndi pamaso pa gulu lonse.
[23] Ndipo anamusanjika manja ndi kumupatsa mphamvu, monga Yehova
ananenera kudzera mwa Mose.

# 28

## *Zopereka za Tsiku ndi Tsiku*

[1] Yehova anawuza Mose kuti, [2] "Lamula Aisraeli kuti, 'Onetsetsani
kuti mukupereka kwa Ine pa nthawi yoyikika, chopereka cha chakudya
chotentha pa moto monga fungo lokoma kwa Ine.' [3] Awuze kuti,
'Nsembe ya chakudya imene muzipereka pa moto kwa Yehova tsiku ndi
tsiku ndi iyi: Ana ankhosa a chaka chimodzi awiri, wopanda chilema.
[4] Mmawa muzipereka mwana wankhosa mmodzi ndipo winayo madzulo.
[5] Muziperekanso kilogalamu imodzi ya ufa wosalala wosakaniza ndi lita
imodzi ya mafuta a olivi. [6] Iyi ndi nsembe yopsereza ya tsiku ndi tsiku
imene analamula pa phiri la Sinai kuti ikhale fungo lokoma, nsembe
yopsereza pa moto yopereka kwa Yehova. [7] Chopereka chachakumwa
chikhale lita imodzi yachakumwa chaukali pa nkhosa iliyonse. Muzithira
pamalo opatulika, kupereka kwa Yehova. [8] Muzipereka mwana wankhosa
winayo madzulo, pamodzi ndi chopereka chachakudya monga poyamba
paja ndi chopereka chachakumwa monga mmawa. Ichi ndi chopereka
chachakudya, fungo lokoma kwa Yehova.' "

## *Zopereka za pa Sabata*

[9] " 'Pa tsiku la Sabata, muzipereka nsembe ana ankhosa awiri a chaka
chimodzi wopanda chilema, pamodzi ndi chopereka chachakumwa ndi
chopereka chachakudya chokwana makilogalamu awiri a ufa wosalala
wosakaniza ndi mafuta. [10] Iyi ndi nsembe yopsereza ya pa Sabata iliyonse,
kuwonjezera pa nsembe yopsereza ya nthawi zonse ndi chopereka chake
chachakumwa.' "

## *Zopereka za pa Mwezi*

[11] "Pa tsiku loyamba la mwezi uliwonse muzipereka kwa Yehova nsembe
yopsereza ya ana ang'ombe aamuna awiri, nkhosa yayimuna imodzi,
ana ankhosa aamuna asanu ndi awiri a chaka chimodzi, onse wopanda
chilema. [12] Pa ng'ombe yayimuna iliyonse pakhale chopereka cha
chakudya cha makilogalamu atatu a ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta;
ndi nkhosa yayimuna, chopereka cha chakudya cha makilogalamu awiri
a ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta; [13] ndipo pa mwana wankhosa
aliyense, chopereka cha ufa wa kilogalamu imodzi ya ufa wosalala
wosakaniza ndi mafuta, izi ndi za nsembe yopsereza, fungo lokoma,
nsembe yotentha pa moto ya kwa Yehova. [14] Pa ng'ombe yayimuna
iliyonse pakhale chopereka cha chakumwa cha malita awiri a vinyo; ndipo
pa nkhosa yayimuna, lita limodzi ndi theka, ndipo pa mwana wankhosa,
lita limodzi. Iyi ndi nsembe yopsereza ya mwezi ndi mwezi yoperekedwa
pa mwezi watsopano m'kati mwa chaka. [15] Powonjezera pa nsembe
yopsereza ya nthawi zonse ndi chopereka chake cha chakumwa, mbuzi
yayimuna imodzi iperekedwe kwa Yehova ngati nsembe yopepesera
machimo.

## *Paska*

[16] " 'Pa tsiku la 14 la mwezi woyamba muzichita Paska wa Yehova. [17] Pa
tsiku la 15 la mwezi womwewo pazikhala chikondwerero. Muzidya buledi

wopanda yisiti kwa masiku asanu ndi awiri. 18 Pa tsiku loyamba muzichita
msonkhano wopatulika ndipo musamagwire ntchito iliyonse. 19 Koma
muzipereka kwa Yehova nsembe yotentha pa moto, nsembe yopsereza ya
ana ang'ombe aamuna awiri, nkhosa yayimuna imodzi ndi ana ankhosa
asanu ndi awiri aamuna a chaka chimodzi, onsewo wopanda chilema.
20 Pamodzi ndi ng'ombe yayimuna iliyonse, muzikonza chopereka cha
chakudya cha makilogalamu atatu a ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta;
makilogalamu awiri pa nkhosa yayimuna iliyonse. 21 Kilogalamu imodzi
pa mwana wankhosa aliyense mwa ana ankhosa asanu ndi awiri aja.
22 Muziphatikizapo mbuzi yayimuna monga nsembe yopepesera machimo
anu. 23 Muzikonza zimenezi nthawi zonse, powonjezera pa nsembe
yopsereza ya mmawa. 24 Motere muzikonza chakudya cha nsembe
yopsereza ya tsiku ndi tsiku pa masiku asanu ndi awiri ngati fungo
lokomera Yehova. Zimenezi ziziperekedwa kuwonjezera pa nsembe
yopsereza ya nthawi zonse pamodzi ndi nsembe yachakumwa. 25 Pa
tsiku lachisanu ndi chiwiri muzichita msonkhano wopatulika ndipo
musamagwire ntchito iliyonse.

### *Madyerero a Masabata*

26 " 'Pa tsiku la zipatso zoyambirira kucha, pamene mukupereka chop-
ereka cha chakudya chatsopano kwa Yehova, pa nthawi ya chikondwerero
cha Masabata, muzichita msonkhano wopatulika ndipo musagwire ntchito
zolemetsa. 27 Muzipereka nsembe zopsereza za ana ang'ombe aamuna
awiri, nkhosa imodzi yayimuna ndi ana ankhosa aamuna asanu ndi
awiri a chaka chimodzi monga fungo lokomera Yehova. 28 Pa ng'ombe
yayimuna iliyonse pazikhala chopereka cha chakudya cha makilogalamu
atatu a ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta, pa nkhosa yayimuna iliyonse
makilogalamu awiri. 29 Ndipo pa mwana wankhosa aliyense mwa asanu
ndi awiri aja, kilogalamu imodzi. 30 Muziperekanso mbuzi yayimuna
imodzi kuti izikhala nsembe yopepesera machimo anu. 31 Muzipereka
zimenezi pamodzi ndi zopereka za zakumwa ndi nsembe yake ya
chakudya. Onetsetsani kuti nyamazo zilibe chilema.

# 29

### *Chikondwerero cha Malipenga*

1 " 'Pa tsiku loyamba la mwezi wachisanu ndi chiwiri muzichita
msonkhano wopatulika ndipo musamagwire ntchito iliyonse. Ili ndi tsiku
limene muziliza malipenga. 2 Muzipereka mwana wang'ombe wamwa-
muna mmodzi, nkhosa yayimuna imodzi ndi ana ankhosa asanu ndi
awiri a chaka chimodzi wopanda chilema monga nsembe zopsereza, fungo
lokoma kwa Yehova. 3 Pa ng'ombe yayimuna iliyonse, muzipereka chop-
ereka cha chakudya cha makilogalamu atatu a ufa wosalala wosakaniza
ndi mafuta. Pa nkhosa yayimuna iliyonse muzipereka makilogalamu
awiri. 4 Pa mwana wankhosa aliyense mwa asanu ndi awiri aja
muzipereka kilogalamu imodzi. 5 Muziperekanso mbuzi yayimuna kuti
izikhala nsembe yopepesera machimo anu. 6 Izi ndi zowonjezera pa
nsembe zopsereza za mwezi ndi mwezi komanso za tsiku ndi tsiku
pamodzi ndi zopereka za chakudya ndi zopereka za chakumwa potsata
malamulo ake. Izi ndi zopereka zotentha pa moto, zoperekedwa kwa
Yehova, fungo lokoma.

### *Tsiku la Mwambo Wopepesera Machimo*

7 " 'Pa tsiku lakhumi la mwezi wachisanu ndi chiwiriwu, muzichita
msonkhano wopatulika. Muzisala zakudya ndipo musamagwire ntchito.
8 Muzipereka kwa Yehova nsembe yopsereza, yotulutsa fungo lokoma
lokondweretsa Yehovayo; ng'ombe yayimuna imodzi, nkhosa yayimuna
imodzi ndi ana ankhosa asanu ndi awiri a chaka chimodzi. Zimenezi
zizikhala zopanda chilema. 9 Pa ng'ombe yayimuna iliyonse, muzikonza
chopereka cha chakudya cha makilogalamu atatu a ufa wosalala
wosakaniza ndi mafuta; pa nkhosa yayimuna iliyonse makilogalamu
awiri; 10 kilogalamu imodzi pa mwana wankhosa aliyense mwa asanu ndi
awiriwo. 11 Muziperekanso mbuzi imodzi yayimuna kuti izikhala nsembe
yopepesera machimo, kuwonjezera pa nsembe yopepesera machimo ya
pa tsiku la mwambo ija, kuwonjezanso pa nsembe zopsereza za tsiku ndi
tsiku zija, pamodzi ndi chopereka chake cha chakudya ndi cha chakumwa.

### *Chikondwerero cha Misasa*

12 " 'Pa tsiku la mwezi wachisanu ndi chiwiri, muzichita msonkhano
wopatulika ndipo musamagwire ntchito iliyonse. Muzichita madyerero
a Yehova masiku asanu ndi awiri. 13 Muzipereka nsembe yotentha
pa moto, kuti izikhala fungo lokoma kwa Yehova, nsembe yopsereza
ya ana ang'ombe aamuna khumi ndi atatu, nkhosa zazimuna ziwiri,
ndi ana ankhosa aamuna khumi ndi anayi a chaka chimodzi, zonse
zopanda chilema. 14 Pa mwana wang'ombe aliyense mwa ana ang'ombe
aamuna khumi ndi atatu aja, muzikonza chopereka cha chakudya cha
makilogalamu atatu a ufa wosalala wosakaniza ndi mafuta. Pa nkhosa
iliyonse mwa nkhosa ziwiri zija, mukonza chopereka cha chakudya cha
makilogalamu awiri. 15 Pa mwana wankhosa aliyense mwa ana ankhosa
aamuna khumi ndi anayiwo, muzipereka chakudya cha kilogalamu
imodzi. 16 Muziperekanso mbuzi yayimuna imodzi kuti izikhale nsembe
yopepesera machimo, kuwonjezera pa nsembe zopsereza za tsiku ndi tsiku
zija pamodzi ndi chopereka chake cha chakudya ndi chakumwa.

17 " 'Pa tsiku lachiwiri muzipereka ana ang'ombe aamuna khumi ndi
awiri aja, nkhosa zazimuna ziwiri ndi ana ankhosa aamuna khumi
ndi anayi a chaka chimodzi aja, zonse zopanda chilema. 18 Pamodzi
ndi ng'ombe zazimuna, nkhosa zazimuna ndi ana ankhosa, muzipereka
zopereka za chakudya ndi za chakumwa molingana ndi chiwerengero
cha nyamazo. 19 Muziperekanso mbuzi imodzi yayimuna ya nsembe
yopepesera machimo powonjezera pa nsembe yopsereza ya tsiku ndi tsiku
pamodzi ndi chopereka chake cha chakudya ndi chakumwa.

20 " 'Pa tsiku lachitatu muzipereka ng'ombe zazimuna khumi ndi imodzi,
nkhosa zazimuna ziwiri ndi ana ankhosa aamuna khumi ndi anayi
a chaka chimodzi, zonse zopanda chilema. 21 Pamodzi ndi ng'ombe
zazimuna, nkhosa zazimuna ndi ana ankhosa, muzipereka zopereka
za chakudya ndi za chakumwa molingana ndi chiwerengero cha nya-
mazo. 22 Muziperekanso mbuzi imodzi yayimuna ya nsembe yopepesera
machimo, powonjezera pa nsembe yopsereza ya tsiku ndi tsiku pamodzi
ndi chopereka chake cha chakudya ndi chakumwa.

23 " 'Pa tsiku lachinayi muzipereka ng'ombe zazimuna khumi, nkhosa
zazimuna ziwiri ndi ana ankhosa aamuna khumi ndi anayi a chaka chi-
modzi, zonse zopanda chilema. 24 Pamodzi ndi ng'ombe zazimuna, nkhosa
zazimuna ndi ana ankhosa, muzipereka chopereka cha chakudya ndi
chakumwa molingana ndi chiwerengero cha nyamazo. 25 Muziperekanso

mbuzi imodzi yayimuna ya nsembe yopepesera machimo, powonjezera
pa nsembe yopsereza ya tsiku ndi tsiku pamodzi ndi chopereka chake cha
chakudya ndi chakumwa.
26 “ ‘Pa tsiku lachisanu muzipereka ng’ombe zazimuna zisanu ndi
zinayi, nkhosa zazimuna ziwiri ndi ana ankhosa aamuna khumi ndi
anayi a chaka chimodzi, zonse zopanda chilema. 27 Pamodzi ndi
ng’ombe zazimuna, nkhosa zazimuna ndi ana ankhosa, muzipereka
chopereka cha chakudya ndi chakumwa molingana ndi chiwerengero
cha nyamazo. 28 Muziperekanso mbuzi imodzi yayimuna ya nsembe
yopepesera machimo, powonjezera pa nsembe yopsereza ya tsiku ndi tsiku
ndi chopereka chake cha chakudya ndi chakumwa.
29 “ ‘Pa tsiku lachisanu ndi chimodzi muzipereka ng’ombe zazimuna
zisanu ndi zitatu, nkhosa zazimuna ziwiri ndi ana ankhosa aamuna
khumi ndi anayi a chaka chimodzi, zonse zopanda chilema. 30 Pamodzi
ndi ng’ombe zazimuna, nkhosa zazimuna ndi ana ankhosa, muzipereka
chopereka cha chakudya ndi cha chakumwa molingana ndi chiwerengero
cha nyamazo. 31 Muziperekenso mbuzi imodzi yayimuna ya nsembe
yopepesera machimo, powonjezera pa nsembe yopsereza ya tsiku ndi tsiku
pamodzi ndi chopereka chake cha chakudya ndi chakumwa.
32 “ ‘Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri muzipereka ng’ombe zazimuna
zisanu ndi ziwiri, nkhosa zazimuna ziwiri ndi ana ankhosa amuna
khumi ndi anayi a chaka chimodzi, zonse zopanda chilema. 33 Pamodzi
ndi ng’ombe zazimuna, nkhosa zazimuna ndi ana ankhosa, muzipereka
chopereka cha chakudya ndi chakumwa molingana ndi chiwerengero
cha nyamazo. 34 Muziperekanso mbuzi imodzi yayimuna ya nsembe
yopepesera machimo, powonjezera pa nsembe yopsereza ya tsiku ndi tsiku
pamodzi ndi chopereka chake cha chakudya ndi chakumwa.
35 “ ‘Pa tsiku lachisanu ndi chitatu muzichita msonkhano ndipo musam-
agwire ntchito iliyonse. 36 Muzipereka chopereka chotentha pa moto
monga fungo lokoma kwa Yehova, nsembe yopsereza ya ng’ombe imodzi
yayimuna, nkhosa yayimuna imodzi ndi ana ankhosa amuna asanu
ndi awiri a chaka chimodzi, zonse zopanda chilema. 37 Pamodzi
ndi ng’ombe yayimunayo, nkhosa yayimunayo ndi ana ankhosawo,
muzipereka chopereka cha chakudya ndi chakumwa molingana ndi
chiwerengero cha nyamazo. 38 Muziperekanso mbuzi imodzi yayimuna ya
nsembe yopepesera machimo, powonjezera pa nsembe yopsereza ya tsiku
ndi tsiku pamodzi ndi chopereka chake cha chakudya ndi chakumwa.
39 “ ‘Kuwonjezera pa zopereka zimene munalumbirira ndi pa zopereka
zanu zaufulu, muzipereka zimenezi kwa Yehova pa masiku osankhika
a chikondwerero chanu. Nsembe zanu zachakumwa ndi nsembe zanu
zachiyanjano.’ ”
40 Mose anawuza Aisraeli zonse zimene Yehova anamulamulira.

# 30

*Za Kulumbira*
1 Mose anawuza Aisraeli onse zonse zimene Yehova anamulamula.
Iye anati, “Zimene Yehova walamula ndi izi: 2 Munthu wamwamuna
ngati walonjeza kwa Yehova kapena kulumbira kuti adzachita zimene
walumbirazo, asaphwanye mawuwo koma ayenera kuchita chilichonse
chimene wanena.
3 “Pamene munthu wamkazi amene akukhalabe m’nyumba ya abambo
ake alumbira kwa Yehova kuti adzachita zimene walonjeza pa ubwana

wake, 4 abambo ake namva kulumbira kwakeko kapena kulonjeza
kwake kuti adzachitadi, ndipo abambo akewo wosayankhula kanthu,
mkaziyo achitedi zomwe analumbirazo. Ayenera kudzachita zonse
zimene walonjeza zija. 5 Koma ngati abambo akewo amva kulumbira
kwake ndi kumukaniza, palibe lamulo lomukakamiza mkaziyo kuchita
zimene walonjeza. Yehova adzamukhululukira chifukwa abambo ake
anamukaniza.

6 "Ngati akwatiwa atalumbira kale kapena ngati alonjeza mofulumira
ndi pakamwa pake, 7 mwamuna wake ndi kumva kulumbira kwakeko
koma wosanenapo kanthu, mkaziyo achitedi zomwe walumbirazo. Achite
ndithu zomwe walonjeza zija. 8 Koma ngati mwamuna wake amuletsa
atamva kulumbira kwakeko, pamenepo amumasula mayiyo ku zimene
analumbira komanso ku zimene analonjeza mosaganiza bwinozo ndipo
Yehova adzamukhululukira.

9 "Mayi wamasiye kapena wosiyidwa ukwati akalumbira kapena kulonjeza kuti adzachita kanthu kalikonse, ayenera kukachitadi.

10 "Koma ngati mayi wokwatiwa alumbira nalonjeza kuti adzachitadi
zimene walonjeza, 11 mwamuna wake ndi kumva kulumbira kwakeko
koma osayankhulapo kanthu, osamuletsa, ayenera kuchitadi zonse zimene
walumbira ndi zonse zimene walonjeza. 12 Koma ngati mwamuna wake
amva ndi kumuletsa kuti asachite zomwe walumbirazo, palibe lamulo
lomukakamiza mayiyo kuchita zomwe walumbirazo kapenanso zimene
walonjeza. Popeza mwamuna wake wamuletsa, Yehova adzamukhululukira mayiyo.
13 Mwamuna wake ali ndi mphamvu zovomereza kapena
kukana zimene mayiyo walumbira kapena zimene walonjeza zokhudza
kudzilanga yekha. 14 Ndipo ngati mmawa mwake ndi masiku otsatira
mwamuna wake sanenapo kanthu atamva zimenezi, mayiyo achitedi
zimene walumbira kapena zimene walonjeza. Mwamunayo wavomereza
zimenezo, chifukwa sanamuwuze kanthu mayiyo pa tsiku limene anamva
akulonjeza kapena kulumbira. 15 Koma ngati mwamunayo amukaniza
patapita kanthawi atazimva kale, iyeyo ndiye wochimwa m'malo mwa
mayiyo."

16 Awa ndiwo malamulo amene Yehova analamula Mose za mwamuna
ndi mkazi wake, ndiponso abambo ndi mwana wawo wamkazi amene
akanali mtsikana wokhalabe m'nyumba ya abambo akewo.

# 31

*Aisraeli Agonjetsa Amidiyani*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Uwabwezere zoyipa Amidiyani chifukwa cha zimene anachitira Aisraeli. Ukatha kuchita zimenezi, iwe
udzamwalira."

3 Ndipo Mose anati kwa Aisraeli, "Perekani zida kwa ena mwa anthu
anu kuti akamenyane ndi Amidiyani ndi kuwabwezera choyipa m'malo
mwa Yehova. 4 Mutumize ku nkhondoko amuna 1,000 kuchokera ku fuko
lililonse la Aisraeli." 5 Choncho amuna okwana 12,000 anatenga zida
kukonzekera nkhondo, anthu 1,000 kuchokera ku fuko lililonse la Aisraeli.
6 Mose anawatumiza ku nkhondo, anthu 1,000 kuchokera ku fuko lililonse
pamodzi ndi Finehasi mwana wa Eliezara wansembe amene ananyamula
zipangizo zochokera ku malo wopatulika ndi malipenga okaliza.

7 Iwo anamenyana ndi Amidiyani monga momwe Yehova analamulira
Mose ndipo anapha mwamuna aliyense. 8 Mwa anthu ophedwawo munali

Evi, Rekemu, Zuri, Huri ndi Reba, mafumu asanu a Amidiyani. Ndipo
anaphanso ndi lupanga Balaamu mwana wa Beori. 9 Aisraeli anagwira
ukapolo amayi a Chimidiyani ndi ana awo ndipo analandanso ng'ombe,
ziweto zawo zina zonse ndi katundu wawo yense. 10 Anawotcha mizinda
yonse imene Amidiyani ankakhalamo pamodzi ndi misasa yawo yonse.
11 Anatenga zonse zimene analanda ku nkhondoko, anthu ndi zoweta
zomwe. 12 Ndipo anabwera nawo akapolowo ndi zolanda ku nkhondozo
kwa Mose ndi kwa wansembe Eliezara ndi kwa gulu lonse la Aisraeli ku
misasa yawo ku chigwa cha Mowabu, m'mbali mwa mtsinje wa Yorodani
ku Yeriko.

13 Mose, wansembe Eliezara ndi atsogoleri onse a gululo anapita
kukakumana nawo kunja kwa misasa. 14 Mose anakwiya nawo akuluakulu
a magulu a ankhondowo: olamulira 1,000 ndi olamulira 100, amene
ankachokera ku nkhondo.

15 Iye anafunsa kuti, "Kodi n'chifukwa chiyani mwawaleka amoyo amayi
onsewa?" 16 Paja iwo ndi amene ankatsatira uphungu wa Balaamu
ndiponso ndi amene anachititsa Aisraeli kuti asiye Yehova pa zimene
zinachitika ku Peori, kotero mliri unagwera anthu a Yehova. 17 Tsopano
iphani munthu wamwamuna aliyense. Ndiponso iphani mayi aliyense
amene anagonapo ndi mwamuna, 18 koma sungani mtsikana aliyense
amene sanagonepo ndi mwamuna.

19 "Inu nonse amene mwaphapo wina wake, kapena kukhudza
aliyense amene anaphedwa mukhale kunja kwa msasa masiku asanu
ndi awiri. Pa tsiku lachitatu mudziyeretse nokha pamodzi ndi akapolo
anu. 20 Muyeretsenso zovala zanu ndi china chilichonse chopangidwa ndi
chikopa, ubweya wa mbuzi kapenanso ndi mtengo."

21 Tsono wansembe Eliezara anati kwa asilikali amene anapita ku
nkhondo aja, "Lamulo limene Yehova anapereka kwa Mose ndi ili:
22 Golide, siliva, mkuwa, chitsulo, chiwaya, mtovu 23 ndi china chili-
chonse chimene sichingapse ndi moto muchidutsitse pa moto, ndipo
chidzayeretsedwa. Komanso chiyeretsedwe ndi madzi oyeretsa. Ndipo
chilichonse chimene chingapse ndi moto muchidutsitse m'madzimo. 24 Pa
tsiku lachisanu ndi chiwiri muchape zovala zanu ndipo mudzayera.
Mukatero mutha kulowa mu msasa."

### *Kugawana Zolanda ku Nkhondo*

25 Yehova anawuza Mose kuti, 26 "Iwe ndi wansembe Eliezara ndiponso
akuluakulu a mabanja a anthuwa, muwerenge anthu onse ndi ziweto
zomwe zinagwidwa ku nkhondo. 27 Mugawe zolanda ku nkhondozo
magawo awiri, lina la ankhondo amene anapita ku nkhondo, lina la anthu
onse. 28 Pa gawo la ankhondowo, mutengeko gawo la Yehova, pa zofunkha
500 zilizonse mutengeko chimodzi, pa akapolo, ng'ombe, bulu ndi nkhosa.
29 Utenge zimenezo pa theka la gawo la ankhondowo ndipo upereke kwa
wansembe Eliezara kuti zikhale zopereka zanu kwa Yehova. 30 Kuchokera
pa theka la gawo la Aisraeli, utengeko cholanda chimodzi pa makumi
asanu aliwonse, pa anthu, ng'ombe, abulu, nkhosa, mbuzi kapena zoweta
zina. Uzipereke kwa Alevi amene ntchito yawo ndi yosamalira tenti ya
Yehova." 31 Ndipo Mose ndi wansembe Eliezara anachita monga Yehova
analamulira Mose.

32 Zotsala pa zolanda ku nkhondo zimene ankhondowo anatenga zinali
nkhosa 675,000, 33 Ng'ombe 72,000, 34 abulu 61,000, 35 ndi atsikana omwe
sanagonepo ndi mwamuna 32,000.

36 Gawo la ankhondo amene anapita ku nkhondo linali:

nkhosa 337,500, 37 mwa zimenezi gawo la Yehova linali 675;
38 ng’ombe zinalipo 36,000 ndipo gawo la Yehova linali 72;
39 abulu analipo 30,500 ndipo gawo la Yehova linali 61;
40 anthu analipo 16,000 ndipo gawo la Yehova linali 32.

41 Mose anapereka kwa wansembe Eliezara gawo limene linali loyenera
kupereka kwa Yehova monga momwe Yehova analamulira Mose.
42 Pa gawo la Aisraeli, Mose anapatula theka limodzi kuchotsa pa
zolanda ku nkhondo zonse zimene zinabwera ndi ankhondo aja. 43 Tsono
gawo la Aisraeli linali ili: nkhosa 337,500, 44 ng’ombe 36,000, 45 abulu
30,500, 46 anthu 16,000. 47 Kuchoka pa gawo la Aisraelilo, Mose anatengapo
chimodzi pa zolanda ku nkhondo makumi asanu aliwonse, anthu ndi
nyama, ndipo anazipereka kwa Alevi amene ankayang’anira tenti ya
Yehova monga Yehova analamulira Mose.
48 Pamenepo omwe ankayang’anira magulu a ankhondo olamulira 1,000
ndi olamulira 100 anabwera kwa Mose, 49 iwo anati kwa iye, “Ife anthu
anu tawerenga ankhondo amene timawalamulira. Palibe munthu ndi
mmodzi yemwe amene wasowa. 50 Ndipo tabweretsa zopereka kwa
Yehova zimene munthu aliyense anapeza: ziwiya zagolide, zibangiri,
zigwinjiri, mphete zosindikizira, ndolo ndi mikanda kuti tichitire mwambo
wopepesera machimo pamaso pa Yehova.”
51 Ndipo Mose ndi wansembe Eliezara analandira kuchokera kwa
atsogoleriwo golide pamodzi ndi zipangizo zonse zosula. 52 Golide
yense wochokera kwa atsogoleri a 1,000 ndi atsogoleri a 100 zomwe
Mose ndi Eliezara anapereka ngati mphatso kwa Yehova zinali zolemera
makilogalamu 200. 53 Wankhondo aliyense anatenga zomwe analanda
yekha ku nkhondo. 54 Mose ndi Eliezara wansembe analandira golide
kuchokera kwa atsogoleri a 1,000 ndi atsogoleri a 100 ndi kukamuyika mu
tenti ya msonkhano ngati chikumbutso cha Aisraeli pamaso pa Yehova.

# 32

*Mafuko a ku Tsidya la Yorodani*

1 Arubeni ndi Agadi amene anali ndi ng’ombe zambiri ndi ziweto zina
anaona dziko la Yazeri ndi la Giliyadi kuti linali labwino kwa ziwetozo.
2 Choncho Arubeni ndi Agadi anapita kwa Mose ndi kwa wansembe
Eliezara ndi kwa atsogoleri a anthu ndi kunena kuti, 3 “Ataroti, Diboni,
Yazeri, Nimira, Hesiboni, Eleali, Sebamu, Nebo ndi Beoni, 4 dziko lomwe
Yehova anagonjetsa pamaso pa Aisraeli, ndiwo malo woyenera ziweto,
ndipo atumiki anufe tili ndi ziweto. 5 Iwo anati, ‘Ngati tapeza ufulu
pamaso panu atumiki anufe, mutipatse dziko limeneli kuti likhale lathu.
Tisawoloke nanu Yorodani.’ ”
6 Ndipo Mose anati kwa Agadi ndi Arubeni, “Kodi anthu a mtundu wanu
apite ku nkhondo inu mutangokhala kuno? 7 Chifukwa chiyani muku-
fowoketsa Aisraeli kupita m’dziko limene Yehova wawapatsa? 8 Izi ndi
zimene makolo anu anachita pamene ndinawatuma kuchokera ku Kadesi
kukaona dzikolo. 9 Atapita ku chigwa cha Esikolo, ndi kuliona dzikolo,
anafowoketsa Aisraeli kuti asalowe m’dziko limene Yehova anawapatsa.
10 Yehova anakwiya tsiku limenelo ndipo analumbira kuti, 11 ‘Chifukwa

sananditsatire ndi mtima wonse, palibe ndi mmodzi yemwe mwa amuna
a zaka makumi awiri kapena kuposa pamenepo, amene anachokera ku
Igupto, amene adzaone dziko limene ndinalonjeza mwa lumbiro kwa
Abrahamu, Isake ndi Yakobo. 12 Palibe ndi mmodzi yemwe kupatula
Kalebe mwana wa Yefune, Mkeni, ndi Yoswa mwana wa Nuni chifukwa
anatsatira Yehova ndi mtima wonse.' 13 Yehova anakwiyira Aisraeli
kwambiri ndipo anawachititsa kuyenda m'chipululu zaka makumi anayi,
mpaka m'bado wonse wa anthu amene anachita choyipa pamaso pake
unatha.

14 "Ndipo onani tsopano, inu m'bado wochimwa, mwalowa m'malo
mwa makolo anu ndipo mwachititsa kuti Yehova akwiyire Israeli
kwambiri. 15 Ngati muleka kumutsata, Iye adzawasiyiranso anthu onsewa
m'chipululu ndipo mudzawonongetsa anthu onsewa."

16 Ndipo iwo anabwera kwa Mose namuwuza kuti, "Ife tikufuna
kumanga makola a ziweto zathu kuno ndi mizinda yokhalamo akazi
athu ndi ana athu. 17 Koma ndife okonzeka kutenga zida za nkhondo
ndi kupita pamodzi ndi Aisraeli mpaka titakawafikitsa ku malo awo.
Panopa, akazi ndi ana athu akhala m'mizinda yotetezedwa, kuwateteza
kwa anthu okhala m'dzikoli. 18 Sitidzabwerera ku midzi yathu mpaka
Mwisraeli aliyense atalandira cholowa chake. 19 Sitidzalandira cholowa
chilichonse pamodzi nawo ku tsidya lina la Yorodani, chifukwa cholowa
chathu tachipezera ku tsidya lino la kummawa kwa Yorodani."

20 Tsono Mose anati kwa anthuwo, "Ngati inu mudzachita zimenezi,
kutenga zida zankhondo pamaso pa Yehova kuti muchite nkhondo,
21 ndipo ngati nonsenu mudzapita ndi zida kuwoloka Yorodani pamaso
pa Yehova mpaka atachotsa adani ake pamaso pake, 22 dzikolo n'kugonja
pamaso pa Yehova, mudzabwera ndi kukhala mfulu pamaso pa Yehova
ndi Aisraeli. Ndipo dziko lino lidzakhala lanu pamaso pa Yehova.

23 "Koma mukalephera kuchita izi, mudzakhala mukuchimwira Yehova.
Ndipo dziwani kuti tchimo lanu lidzakupezani. 24 Amangireni akazi ndi
ana anu mizinda, mangani makola a ziweto zanu, koma chitani zomwe
mwalonjeza."

25 Agadi ndi Arubeni anati kwa Mose, "Ife antchito anu tidzachita monga
mbuye wathu mwalamulira. 26 Ana ndi akazi athu, ziweto zathu zina
ndi ng'ombe zidzatsala kuno ku mizinda ya Giliyadi, 27 koma antchito
anufe, mwamuna aliyense amene ali ndi chida cha nkhondo, adzawoloka
kukamenya nkhondo pamaso pa Yehova monga mbuye wathu wanenera."

28 Choncho Mose anapereka malamulo awa kwa wansembe Eliezara,
kwa Yoswa mwana wa Nuni ndi kwa akulu a mafuko a Aisraeli.
29 Mose anawawuza kuti, ngati Agadi ndi Arubeni, mwamuna aliyense
wokonzekera nkhondo, awoloka Yorodani pamodzi ndi inu pamaso pa
Yehova, ndipo dzikolo n'kugonjetsedwa pamaso panu, mudzawapatse
dziko la Giliyadi kukhala lawo. 30 Koma ngati sawoloka pamodzi nanu
ndi zida zankhondo, ayenera kulandira cholowa chawo pamodzi ndi inu
ku Kanaani.

31 Agadi ndi Arubeni anayankha kuti, "Antchito anu adzachita zimene
Yehova wanena. 32 Tidzawoloka pamaso pa Yehova ndipo tidzalowa mu
Kanaani ndi zida zankhondo, koma cholowa chathu chidzakhala ku tsidya
lino la Yorodani."

33 Choncho Mose anapatsa Agadi, Arubeni ndi theka la fuko la Manase
mwana wa Yosefe dziko la Sihoni mfumu ya Aamori ndi dziko la Ogi,
mfumu ya ku Basani, dziko lonse, mizinda yake ndi midzi yowazungulira.
34 Agadi anamanga Diboni, Ataroti, Aroeri, 35 Atiroti-Sofani, Yazeri, Yo-
gibeha, 36 Beti-Nimira ndi Beti-Harani mizinda ya malinga. Anamanganso
makola a ziweto zawo. 37 Ndipo Arubeni anamanga Hesiboni, Eleali,
Kiriataimu, 38 Nebo ndi Baala-Meoni (mayina awa anasinthidwa) ndi
Sibima. Anapereka mayina ku mizinda ina yomwe anamangayo.
39 Zidzukulu za Makiri mwana wa Manase zinapita ku Giliyadi kulanda
mzindawo ndi kuthamangitsira kunja Aamori omwe anali kumeneko.
40 Tsono Mose anapereka Giliyadi kwa Amakiri, ana a Manase, ndipo
anakhala kumeneko. 41 Yairi, mwana wa Manase analanda midzi yambiri
ya Giliyadi ndi kuyitcha kuti Havoti-Yairi. 42 Ndipo Noba analanda Kenati
ndi midzi yozungulira ndi kuyitcha Noba, kutengera dzina la iye mwini.

# 33

*Malo omwe Aisraeli Anayima pa Ulendo Wawo*

1 Malo otsatirawa ndi omwe Aisraeli anayima pa maulendo awo
atatuluka m'dziko la Igupto m'magulu awo motsogozedwa ndi Mose
ndi Aaroni. 2 Mose analemba malo amene anayambira maulendo awo
molamulidwa ndi Yehova. Maulendo awo ndi malo omwe anayambira
ndi awa:

3 Aisraeli ananyamuka kuchokera ku Ramesesi pa tsiku la 15 la mwezi
woyamba, itangotha Paska. Iwo anatuluka nayenda molimba mtima
Aigupto onse akuona, 4 pamene ankayika maliro a ana awo oyamba
kubadwa, omwe Yehova anawakantha pakati pawo chifukwa Yehova
anaweruza milungu yawo.

5 Aisraeli atachoka ku Ramesesi, anamanga misasa yawo ku Sukoti.

6 Atachoka ku Sukoti anakamanga misasa yawo ku Etamu, m'mbali
mwa chipululu.

7 Ndipo atachoka ku Etamu, anabwerera ku Pihahiroti, kummawa kwa
Baala-Zefoni, ndipo anamanga misasa yawo pafupi ndi Migidoli.

8 Atachoka ku Pihahiroti anadutsa m'kati mwa nyanja kupita ku chip-
ululu ndipo atayenda masiku atatu m'chipululu cha Etamu, anamanga
misasa yawo ku Mara.

9 Atachoka ku Mara anafika ku Elimu, kumene kunali akasupe a madzi
khumi ndi awiri ndi mitengo ya migwalangwa 70 ndipo anamanga
misasa yawo kumeneko.

10 Atachoka ku Elimu anakamanga misasa yawo m'mbali mwa Nyanja
Yofiira.

11 Atachoka ku Nyanja Yofiira anakamanga misasa yawo m'chipululu
cha Sini.

12 Atachoka ku chipululu cha Sini anakamanga ku Dofika.

13 Atachoka ku Dofika anakamanga misasa yawo ku Alusi.

14 Atachoka ku Alusi anakamanga misasa yawo ku Refidimu, kumene
kunalibe madzi woti anthu ndi kumwa.

15 Atachoka ku Refidimu anakamanga ku chipululu cha Sinai

16 Atachoka ku chipululu cha Sinai anakamanga misasa yawo ku
Kiburoti-Hataava.

17 Atachoka ku Kiburoti-Hataava anakamanga misasa yawo ku Heziroti.
18 Atachoka ku Heziroti anakamanga ku Ritima.
19 Atachoka ku Ritima anakamanga ku Rimoni-Perezi.
20 Atachoka ku Rimoni-Perezi anakamanga ku Libina.
21 Atachoka ku Libina anakamanga ku Risa.
22 Atachoka ku Risa anakamanga ku Kehelata.
23 Atachoka ku Kehelata anakamanga ku phiri la Seferi.
24 Atachoka ku phiri la Seferi anakamanga ku Harada.
25 Atachoka ku Harada anakamanga ku Mekheloti.
26 Atachoka ku Mekheloti anakamanga ku Tahati.
27 Atachoka ku Tahati anakamanga ku Tera.
28 Atachoka ku Tera anakamanga ku Mitika.
29 Atachoka ku Mitika anakamanga ku Hasimona.
30 Atachoka ku Hasimona anakamanga ku Moseroti.
31 Atachoka ku Moseroti anakamanga ku Beni Yaakani.
32 Atachoka ku Beni Yaakani anakamanga ku Hori-Hagidigadi.
33 Atachoka ku Hori-Hagidigadi anakamanga ku Yotibata.
34 Atachoka ku Yotibata anakamanga ku Abirona.
35 Atachoka ku Abirona anakamanga ku Ezioni-Geberi.
36 Atachoka ku Ezioni-Geberi anakamanga ku Kadesi, m'chipululu cha Zini chimene ndi Kadesi.
37 Anachoka ku Kadesi ndi kukamanga ku phiri la Hori, m'malire
mwa dziko la Edomu. 38 Molamulidwa ndi Yehova, wansembe Aaroni
anakwera ku phiri la Hori kumene anakamwalirira pa tsiku loyamba
la mwezi wachisanu, m'chaka cha makumi anayi, Aisraeli atatuluka
m'dziko la Igupto. 39 Aaroni anamwalira pa phiri la Hori ali ndi zaka
123.
40 Mfumu ya Akanaani ya ku Aradi yomwe inkakhala ku Negevi kummwera kwa Kanaani, inamva kuti Aisraeli akubwera.
41 Atachoka ku phiri la Hori anakamanga ku Zalimoni.
42 Atachoka ku Zalimoni anakamanga ku Punoni.
43 Atachoka ku Punoni anakamanga ku Oboti.
44 Atachoka ku Oboti anakamanga ku Iye-Abarimu.
45 Atachoka ku Iye-Abarimu anakamanga ku Diboni Gadi.
46 Atachoka ku Diboni Gadi anakamanga ku Alimoni-Dibulataimu.
47 Atachoka ku Alimoni-Dibulataimu anakamanga m'mapiri a Abarimu, pafupi ndi Nebo.
48 Atachoka ku mapiri a Abarimu anakamanga ku zigwa za Mowabu
m'mbali mwa Yorodani moyang'anana ndi Yeriko. 49 Ali ku zigwa za
Mowabu anamanga m'mbali mwa Yorodani kuchokera ku Beti-Yesimoti
mpaka ku Abeli-Sitimu.

50 Pa zigwa za Mowabu, m'mbali mwa Yorodani moyang'anana ndi ku
Yeriko, Yehova anawuza Mose kuti, 51 "Nena kwa Aisraeli kuti, 'Pamene
muwoloka Yorodani kulowa m'dziko la Kanaani, 52 mukathamangitse
nzika zonse za m'dzikomo pamaso panu. Mukawononge mafano awo onse
a miyala ndi osula ndi malo awo achipembedzo. 53 Mukalande dzikolo
ndi kukhalamo chifukwa ndakupatsani dziko limenelo kuti mukhalemo.
54 Mukagawane dzikolo pochita maere monga mwa mafuko anu. Kwa

omwe ali ambiri, cholowa chambiri, ndipo amene ali ocheperapo,
chocheperanso. Chilichonse chimene chidzawagwere iwo mwa maere
chidzakhala chawo. Mukaligawane monga mwa mafuko a makolo anu.
55 " 'Koma ngati simukathamangitsa nzika zimene zili m'dzikomo,
amene mukawalole kukhalamo adzakhala ngati zisonga m'maso mwanu
ndi ngati minga m'mbali mwanu. Adzakubweretserani mavuto m'dziko
limene mudzakhalemolo. 56 Ndipo pamenepo ndidzachitira inu zomwe
ndinaganiza kuwachitira iwowo.' "

# 34

*Malire a Dziko la Kanaani*

1 Yehova anawuza Mose kuti, 2 "Lamula Aisraeli ndipo uwawuze kuti,
'Pamene mulowa m'dziko la Kanaani, dziko lomwe lidzaperekedwa kwa
inu ngati cholowa chanu, lidzakhale ndi malire awa:

3 " 'Chigawo cha kummwera kwa dziko lanu chidzayambira ku chipululu
cha Zini motsatana ndi malire a Edomu. Kummawa malire anu a
kummwera adzayambira kummawa, kumathero a Nyanja ya Mchere.
4 Malirewo adzapita kummwera ndipo adzakwera phiri la Akirabimu
mpaka ku Zini. Mathero ake adzakhala kummwera kwa Kadesi-Baranea.
Ndipo adzapitenso ku Hazari Adari mpaka kukafika ku Azimoni, 5 kumene
malirewo adzakhote kuchokera ku Azimoni mpaka ku khwawa la ku
Igupto ndi kukathera ku Nyanja Yayikulu.
6 " 'Malire anu a ku madzulo adzakhala ku gombe la Nyanja Yayikulu.
Amenewo ndiwo adzakhale malire anu a ku madzulo.
7 " 'Malire anu a kumpoto, mzere wake uyambire ku Nyanja Yayikulu
mpaka ku phiri la Hori 8 ndi kuchokera ku phiri la Hori mpaka ku Lebo
Hamati. Malirewa apite ku Zedadi, 9 ndi kupitirira mpaka ku Ziforoni ndi
kukathera ku Hazari-Enani. Awa ndiwo adzakhale malire anu a kumpoto.
10 " 'Za malire anu a kummawa, mulembe mzere kuchokera ku Hazari-
Enani mpaka kukafika ku Sefamu. 11 Malirewo adzatsikire ku Sefamu
mpaka ku Ribila cha kummawa kwa Aini ndi kupitirira mpaka ku matsitso
a cha kummawa kwa Nyanja ya Kinereti. 12 Tsono malirewo adzatsika
motsatana ndi Yorodani ndi kukathera ku Nyanja ya Mchere.
" 'Limeneli lidzakhala dziko lanu ndi malire ake mbali zonse.' "

13 Ndipo Mose analamula Aisraeli kuti, "Limeneli ndi dziko limene
mudzalilandira pochita maere kuti likhale cholowa chanu. Yehova
analamula kuti liperekedwe ku mafuko asanu ndi anayi ndi theka,
14 chifukwa mabanja a fuko la Rubeni, fuko la Gadi, ndi theka la fuko
la Manase analandiriratu cholowa chawo. 15 Mafuko awiriwa pamodzi
ndi theka la fuko la Manase analandiriratu cholowa chawo patsidya pa
mtsinje wa Yorodani ku Yeriko cha kummawa kotulukira dzuwa."
16 Yehova anawuza Mose kuti, 17 "Awa ndi mayina a anthu amene
adzakugawireni dzikoli kuti likhale cholowa chanu: wansembe Eliezara
ndi Yoswa mwana wa Nuni. 18 Musankhe mtsogoleri mmodzi kuchokera
ku fuko lililonse kuti athandize kugawa dzikolo. 19 Mayina awo ndi awa:

Kalebe mwana wa Yefune,
wochokera ku fuko la Yuda,
20 Semueli mwana wa Amihudi,

wochokera ku fuko la Simeoni;
21 Elidadi mwana wa Kisiloni,
wochokera ku fuko la Benjamini;
22 Buki mwana wa Yogili,
mtsogoleri wochokera ku fuko la Dani;
23 Hanieli mwana wa Efodi,
mtsogoleri wochokera ku fuko la Manase, mwana wa Yosefe;
24 Kemueli mwana wa Sifitani,
mtsogoleri wochokera ku fuko la Efereimu, mwana wa Yosefe.
25 Elizafani mwana wa Parinaki,
mtsogoleri wochokera ku fuko la Zebuloni;
26 Palitieli mwana wa Azani,
mtsogoleri wochokera ku fuko la Isakara,
27 Ahihudi mwana wa Selomi,
mtsogoleri wochokera ku fuko la Aseri;
28 Pedaheli mwana wa Amihudi,
mtsogoleri wochokera ku fuko la Nafutali.”

29 Awa ndiwo mayina a anthu amene Yehova analamula kuti agawe cholowa cha Aisraeli m’dziko la Kanaani.

# 35

*Midzi ya Alevi*

1 Ku zigwa za Mowabu pafupi ndi Yorodani ku Yeriko, Yehova anawuza
Mose kuti, 2 “Lamula Aisraeli kuti apereke kwa Alevi midzi yoti azikha-
lamo kuchokera pa cholowa chomwe adzalandira. Muwapatsenso malo
oweteramo ziweto kuzungulira midziyo. 3 Midziyo idzakhala yawo ndipo
azidzakhala m’menemo. Malo a msipu adzakhala a ng’ombe, nkhosa ndi
zoweta zawo zina zonse.
4 “Malo a msipu a mudziwo amene mudzawapatse Aleviwo, adzayam-
bire ku khoma la mudzi ndipo adzatuluke kunja mamita 450, kuzungulira
mudziwo. 5 Kunja kwa mudzi yezani mamita 900 kummawa, mamita 900
kumpoto ndipo mudziwo ukhale pakati. Adzakhala ndi dera limeneli ngati
malo a midziyo, owetera ziweto zawo.

*Mizinda Yopulumukirako*

6 “Isanu ndi umodzi mwa midzi imene mudzapereke kwa Alevi
idzakhala mizinda yopulumukirako, kumene munthu wopha mnzake
adzathawireko. Ndipo mudzawapatsenso midzi ina 42. 7 Midzi yonse
imene mudzapereke kwa Alevi idzakhale 48, pamodzi ndi malo oweterako
ziweto. 8 Pamene mukupatula midzi imeneyi pa cholowa cha Aisraeli,
muchotsepo midzi yambiri pa mafuko aakulu, ndipo midzi pang’ono pa
mafuko aang’ono. Fuko lililonse lidzapereka kwa Alevi molingana ndi
kukula kwa cholowa chimene lalandira.”
9 Ndipo Yehova anawuza Mose kuti, 10 “Yankhula ndi Aisraeli
kuti, ‘Pamene muwoloka Yorodani kulowa mu Kanaani, 11 sankhani
midzi ina kuti ikhale mizinda yanu yopulumukirako, kumene munthu
wopha munthu wina mwangozi angathawireko. 12 Adzakhala malo
obisalako pothawa munthu wofuna kulipsira, kuti munthu wopha mnzake
mwangozi asaphedwe mpaka akayime pamaso pa gulu la anthu kuti
akaweruzidwe. 13 Midzi isanu ndi umodzi imene muyiperekeyi idzakhala
mizinda yopulumukirako. 14 Mupereke itatu mbali ino ya Yorodani ndi

itatu ina mu Kanaani kuti ikhale mizinda yopulumukirako. 15 Midzi isanu
ndi umodzi idzakhala malo opulumukirako Aisraeli, alendo ndi anthu ena
onse okhala pakati pawo kuti wina aliyense wopha mnzake mwangozi
adzathawireko.

16 “ ‘Ngati munthu amenya mnzake ndi chitsulo, munthuyo n’kufa, ndiye
kuti iyeyo ndi wakupha ndipo wakuphayo aphedwe. 17 Kapenanso ngati
wina wake ali ndi mwala m’dzanja mwake womwe ungaphe munthu,
ndipo agenda nawo wina, munthu winayo n’kufa, ndiye kuti iyeyo ndi
wakupha ndipo wakuphayo adzayenera kuphedwa. 18 Kapenanso ngati
wina ali ndi chibonga m’dzanja mwake choti n’kupha nacho munthu,
namenya nacho munthu, munthuyo n’kufa, ndiye kuti iyeyo ndi wakupha,
wakuphayo ayenera kuphedwa. 19 Wolipsira adzamuphanso wakuphayo.
Pamene akumana naye adzayenera kumupha ndithu. 20 Ndipo ngati
wina wake, chifukwa cha udani, aganiza zokankha munthu wina kapena
kumuponyera chinthu china mwadala munthuyo n’kufa, 21 kapena ngati,
chifukwa cha udani, amenya mnzake ndi nkhonya, mnzakeyo ndi kufa,
munthuyo ayenera kuphedwa. Iyeyo ndi wakupha. Wolipsira adzamuphe
wakuphayo pamene akumana naye.

22 “ ‘Koma ngati popanda udani wina uliwonse, mwadzidzidzi akankha
wina kapena kumuponyera chinthu osati mwadala, 23 kapena mosamuona
n’kumuponyera mwala womwe utha kumupha, munthuyo n’kufa, tsono
pakuti sanali mdani wake ndipo sanaganizire zomupweteka, 24 gulu
liweruze pakati pa iye ndi wolipsira monga mwa malamulo ake. 25 Gulu
lidzapulumutsa munthu wakuphayo m’manja mwa wolipsira uja ndi
kumubwezera ku mzinda wopulumukirako kumene anathawira. Ayenera
kukhala kumeneko kufikira imfa ya mkulu wa ansembe, amene anad-
zozedwa ndi mafuta oyera.

26 “ ‘Koma ngati wolakwayo atuluka kunja kwa malire a mzinda wopulu-
mukirako kumene anathawira 27 ndipo wobwezera choyipa n’kumupeza
kunja kwa mzindawo, wolipsirayo atha kumupha wolakwayo popanda
kugamula mlandu wakupha. 28 Wolakwayo ayenera kukhala mu mzinda
wopulumukiramowo mpaka imfa ya mkulu wa ansembe ndipo pamenepo
atha kubwerera kwawo. Pokhapokha atafa mkulu wa ansembe ndi
pamene angathe kubwerera ku malo ake.

29 “ ‘Amenewa akhale malamulo ndi malangizo kwa inu nthawi zonse
ndi ku mibado ya m’tsogolo, kulikonse kumene mudzakhalako.

30 “ ‘Aliyense wopha munthu ayeneranso kuphedwa ngati pali umboni
okwanira. Koma wina asaphedwe ngati pali mboni imodzi yokha.

31 “ ‘Osalola kulandira dipo lowombolera munthu wakupha yemwe
ayenera kuphedwa. Wakupha ayenera kuphedwa.

32 “ ‘Simuyeneranso kulandira dipo kwa munthu amene wathawira ku
mzinda wopulumikirako kuti wothawayo abwerere kwawo, pokhapokha
ngati mkulu wa ansembe wamwalira.

33 “ ‘Musayipitse dziko limene mukukhalamolo. Magazi amayipitsa
dziko ndipo n’kosatheka kulipirira dziko chifukwa cha magazi amene
akhetsedwa m’menemo, kupatula pokhetsa magazi a munthu amene
anakhetsa magaziyo. 34 Choncho musadetse dziko limene mukukhalamo,
dziko limene Inenso ndimakhalamo, pakuti Ine Yehova, ndimakhala pakati
pa Aisraeli.’ ”

# 36

*Cholowa cha Ana Aakazi a Zelofehadi*

1 Atsogoleri a mabanja a fuko la Giliyadi, mwana wa Makiri, mwana wa Manase omwe anali ochokera ku fuko la ana a Yosefe anabwera ndi kuyankhula ndi Mose, atsogoleri ndi akuluakulu a mabanja a Aisraeli.
2 Iwo anati, "Pamene Yehova analamula mbuye wanga kuti apereke dziko ngati cholowa kwa Aisraeli mwa maere, anakulamulani inu kupereka cholowa cha m'bale wathu Zelofehadi kwa ana ake aakazi. 3 Tsopano ngati
akwatiwa ndi aamuna ochokera ku mafuko ena a mitundu ya Aisraeli, cholowa chawo chidzatengedwa kuchoka pa cholowa cha makolo athu ndipo adzachiwonjezera ku fuko limene akwatiwakolo. Ndipo gawo lina
la cholowacho, lopatsidwa kwa ife lidzatengedwa. 4 Pamene chaka cha
chikondwerero cha zaka makumi asanu, cha Aisraeli chafika, cholowa chawo chidzawonjezeredwa ku fuko limene iwo akwatiwako. Ndipo katundu wawo adzachotsedwa pa cholowa cha fuko la makolo athu."

5 Tsono mwa lamulo la Yehova, Mose anapereka lamulo ili kwa Aisraeli:
"Zimene ana a Yosefe akunena ndi zoona. 6 Izi ndi zimene Yehova
akulamula kwa ana aakazi a Zelofehadi: Atha kukwatiwa ndi aliyense amene angakondweretsedwe naye koma zingakhale bwino atakwatiwa
m'fuko la abambo awo 7 kuti cholowa cha Israeli chisapite ku fuko lina,
pakuti Mwisraeli aliyense ayenera kusunga cholowa cha fuko la makolo
ake. 8 Mwana wamkazi aliyense amene adzalandira cholowa cha dziko
la fuko lililonse la Israeli ayenera kukwatiwa ndi munthu wa fuko la
abambo ake. 9 Cholowa chilichonse mu Israeli sichiyenera kupita ku fuko
lina, popeza fuko lililonse la Israeli liyenera kusunga cholowa chimene linalandira."

10 Choncho ana aakazi a Zelofehadi anachita monga Yehova analamulira
Mose. 11 Ana aakazi a Zelofehadi amene ndi Mahila, Tiriza, Hogila, Milika ndi Nowa, anakwatiwa ndi asuweni awo a ku mbali ya abambo awo.
12 Anakwatiwa m'mafuko a zidzukulu za Manase mwana wa Yosefe, ndipo
cholowa chawo chinakhalabe m'fuko la abambo awo.

13 Awa ndi malamulo ndi malangizo amene Yehova anapereka kwa Aisraeli kupyolera mwa Mose ku chigwa cha Mowabu m'mbali mwa Yorodani, ku Yeriko.

# Deuteronomo

*Mose Akumbutsa Aisraeli za ku Horebu*

1 Awa ndi mawu amene Mose anayankhula kwa Aisraeli onse
m'chipululu kummawa kwa Yorodani, ku Araba moyang'anana ndi Sufi,
pakati pa Parani ndi Tofeli, Labani, Heziroti ndi Dizahabu. 2 (Kuyenda
kuchokera ku Horebu kukafika ku Kadesi Barinea kudzera njira ya ku
Phiri la Seiri ndi ulendo wa masiku khumi ndi limodzi).

3 M'chaka cha makumi anayi, pa tsiku loyamba la mwezi 11, Mose
anafotokozera Aisraeli zonse zimene Yehova anamulamula zokhudza
iwowo. 4 Apa n'kuti atagonjetsa Sihoni mfumu ya Aamori, amene
amalamulira ku Hesiboni, ndipo pa Ederi anagonjetsa Ogi mfumu ya ku
Basani, amene amalamulira mu Asiteroti.

5 Chakummawa kwa Yorodani m'chigawo cha Mowabu, Mose anayamba
kufotokozera lamulo ili kunena kuti:

6 Ku Horebu, Yehova Mulungu wathu anati kwa ife, "Mwakhalitsa pa
phiri lino. 7 Sasulani msasa ndipo pitani ku dziko la mapiri la Aamori.
Pitani kwa anthu onse oyandikana nawo ku Araba, ku mapiri, m'mbali
mwa mapiri a ku madzulo, ku Negevi ndiponso m'mbali mwa nyanja,
ku dziko la Akanaani ndi ku Lebanoni mpaka ku mtsinje waukulu wa
Yufurate. 8 Taonani, Ine ndakupatsani dziko ili. Lowani ndi kulilanda
dziko limene Yehova analumbira kuti adzapereka kwa makolo anu,
Abrahamu, Isake ndi Yakobo komanso kwa zidzukulu zawo."

*Kukhazikitsa Atsogoleri*

9 Pa nthawi imeneyi ine ndinati kwa inu, "Inu ndinu katundu olemera
kwambiri woti sindingathe kumunyamula ndekha. 10 Yehova Mulungu
wanu wakuchulukitsani kotero kuti lero lino ndinu ochuluka ngati
nyenyezi za kumwamba. 11 Yehova Mulungu wa makolo anu wachulukitsa
chiwerengero chanu ndipo wakudalitsani monga momwe analonjezera!
12 Koma nanga ndekha ndidzasenza bwanji zovuta ndi zipsinjo zanu
komanso milandu yanu? 13 Sankhani amuna ena anzeru, ozindikira ndi
amene mumawalemekeza kuchokera ku mtundu uliwonse wa mitundu
yanu, ndipo ndidzawayika kuti akulamulireni."

14 Inu munandiyankha kuti, "Maganizo amenewa ndi abwino kuwa-
chita."

15 Choncho ndinatenga anthu otsogolera mafuko anu, anzeru ndi omwe
mumawalemekeza, ndipo ndinawayika kuti azikulamulirani m'magulu
a 1,000, ena 100, ena makumi asanu ndi ena khumi, kuti akhalenso
ngati akapitawo a mafuko. 16 Ndipo pa nthawi imeneyo ndinawawuza
olamula anu kuti, "Muzimva milandu ya pakati pa abale anu ndi kuweruza
mosakondera, kaya mlanduwo uli pakati pa Aisraeli okhaokha kapena
mmodzi wa iwo ndi mlendo. 17 Osamayang'ana nkhope poweruza koma
muzimvetsera aang'ono ndi aakulu omwe chimodzimodzi. Musamaope
munthu aliyense, pakuti chiweruzo ndi cha Mulungu. Muzindibweretsera
mlandu uliwonse wovuta ndipo ndidzaumva." 18 Ndipo nthawi imeneyo
ndinakuwuzani chilichonse chimene munayenera kuchita.

*Atumizidwa Kukazonda Dziko*

19 Tsono monga Yehova Mulungu wathu anatilamulira, tinanyamuka
kuchoka ku Horebu ndi kupita cha ku dziko lamapiri la Aamori kudzera
ku chipululu chachikulu ndi choopsa chija munachionachi, kotero kuti
tinakafika ku Kadesi Barinea. 20 Ndipo ndinati kwa inu, "Mwafika ku
dziko la mapiri la Aamori, limene Yehova Mulungu wathu akutipatsa.
21 Taonani, Yehova Mulungu wanu wakupatsani dzikoli. Pitani ndi
kulitenga monga Yehova, Mulungu wa makolo anu anakuwuzirani.
Musaope kapenanso kugwa mphwayi."

22 Tsono nonse munabwera kwa ine ndi kuti, "Tiyeni titumize anthu
ayambe apita kuti akazonde dzikolo ndi kutibweretsera mawu pa za njira
yomwe tidzere ndi za mizinda imene tikafikireko."

23 Ndinaona kuti maganizo amenewa anali abwino, choncho ndi-
nasankha anthu khumi ndi awiri, mmodzi ku fuko lililonse. 24 Iwo
ananyamuka napita m'dziko la mapiri, ndipo anafika ku Chigwa cha
Esikolo ndi kukazonda dzikolo. 25 Pobwerera anatitengerako zipatso za
m'dzikomo ndipo anatipatsa mawu akuti, "Dziko limene Yehova Mulungu
wathu akutipatsa ndi labwino."

### *Awukira Yehova*

26 Koma inu simunafune kupitako ndipo munawukira lamulo la Yehova
Mulungu wanu. 27 Inu munanyinyirika m'matenti anu n'kumati, "Mu-
lungu amatida n'chifukwa chake anatitulutsa ku Igupto kuti atipereke
m'manja mwa Aamori kuti atiwononge. 28 Tigwire mtengo wanji? Abale
athu anatitayitsa mtima. Iwo akuti, 'Anthuwo ndi amphamvu ndi aatali
kuposa ife, mizindayo ndi yayikulu ndipo mipanda yake ndi yayitali yofika
kumwamba. Ife tinaonanso Aanaki kumeneko.' "

29 Ndipo ine ndinati kwa inu, "Musachite mantha kapena kuwaopa.
30 Yehova Mulungu wanu, amene akukutsogolerani, adzakumenyerani
nkhondo monga muja anachitira ku Igupto inu mukuona, 31 ndi
m'chipululu muja. Kumeneko munaona mmene Yehova Mulungu wanu
anakunyamulirani monga abambo anyamulira mwana wawo, njira yonse
yomwe munayenda mpaka munafika pamalo ano."

32 Ngakhale zinali choncho, simunadalire Yehova Mulungu wanu
33 amene anakutsogolerani pa ulendo wanu, ndi moto nthawi ya usiku
ndi mtambo nthawi ya masana, kukufunirani malo woti mumange msasa
ndi kukuonetsani njira yoti muyendemo.

34 Yehova atamva zimene munanena anakwiya nalumbira kuti,
35 "Palibe ndi mmodzi yemwe mwa m'bado woyipawu amene adzaona
dziko labwino limene ndinalumbira kupatsa makolo anu, 36 kupatula
Kalebe mwana wa Yefune. Iye adzaliona, ndipo ndidzamupatsa iye ndi
adzukulu ake, dziko limene adzapondamo popeza anatsata Yehova ndi
mtima wake wonse."

37 Chifukwa cha inu, Yehova anakwiyiranso ine ndipo anati, "Iwenso
sudzalowa m'dzikomo. 38 Koma Yoswa mwana wa Nuni amene
amakuthandiza, adzalowa m'dzikomo. Umulimbikitse chifukwa adzat-
sogolera Israeli kukalandira dzikolo. 39 Ndipo ang'onoang'ono amene
munati adzagwidwa ukapolo, ana anu amene sanadziwe kusiyanitsa
chabwino ndi choyipa, amenewo adzalowa m'dzikolo. Ndidzalipereka
kwa iwo ndipo lidzakhala lawo. 40 Koma inu, tembenukani nyamukani
kulowera cha ku chipululu kutsatira njira ya ku Nyanja Yofiira."

41 Ndipo inuyo munati, “Tachimwa pamaso pa Yehova. Tipita ndi kuka-
chita nkhondo monga Yehova Mulungu wathu watilamulira.” Choncho
aliyense wa inu anavala zankhondo, ndi kuganiza kuti n’kosavuta kupita
m’dziko la mapiri lija.

42 Koma Yehova anandiwuza kuti, “Awuze anthuwa kuti, ‘Musapite
kukachita nkhondo chifukwa Ine sindidzakhala nanu. Mudzagonjetsedwa
ndi adani anu.’ ”

43 Choncho ndinakuwuzani koma simunamve. Inu munawukira lamulo
la Yehova ndipo mwamwano munayenda kulowa m’dziko la mapiri.
44 Aamori amene ankakhala m’mapiriwo anatuluka kukakumana nanu
ndipo anakuthamangitsani ngati gulu la njuchi ndipo anakukanthani
kuchokera ku Seiri, njira yonse mpaka ku Horima. 45 Munabwererako
mukulira pamaso pa Yehova, koma Iye sanalabadire kulira kwanuko ndipo
sanakumvetsereni. 46 Pamenepo munakhala ku Kadesi masiku ambiri kwa
nthawi yayitali ndithu.

# 2

*Kuyendayenda M’chipululu*

1 Kenaka tinabwerera ndi kuyamba ulendo wolowera ku chipululu
motsatira njira ya ku Nyanja Yofiira, monga mmene Yehova anatilamulira.
Kwa nthawi yayitali tinayendayenda cha ku dziko la mapiri la Seiri.

2 Ndipo Yehova anati kwa ine, 3 “Mwazungulira mokwanira dziko la
mapiri, tsopano tembenukirani kumpoto. 4 Apatse anthu malamulo awa:
‘Muli pafupi kudutsa m’chigawo cha abale anu adzukulu a Esau okhala
ku Seiri. Iwowa adzachita nanu mantha koma musamale kwambiri.
5 Musayambane nawo popeza sindidzakupatsani gawo lina lililonse la
dziko lawo ngakhale poti mungoyika phazi. Ndamupatsa Esau dziko
lamapiri la Seiri kuti likhale lakelake. 6 Inu muyenera kuwalipira ndi siliva
pa chakudya chimene mudye ndi madzi amene mumwe.’ ”

7 Yehova Mulungu wanu wakudalitsani m’ntchito zonse za manja anu.
Iye wakuyang’anirani pa ulendo wanu wodutsa m’chipululu chachikulu.
Yehova Mulungu wanu wakhala nanu m’zaka makumi anayi, ndipo
simunasowe kalikonse.

8 Choncho tinapitiriza ulendo modutsa abale athu, adzukulu a Esau
okhala ku Seiri. Tinapatukira njira ya ku Araba imene imachokera ku Elati
ndi Ezioni Geberi ndipo tinayenda njira ya ku chipululu cha Mowabu.

9 Ndipo Yehova anati kwa ine, “Musawavutitse Amowabu kapena
kuwaputa kuti muchite nawo nkhondo popeza sindidzakupatsani gawo
lina lililonse la dziko lawo. Ndinapereka Ari kwa adzukulu a Loti ngati
chuma chawo.”

10 (Aemi, anthu amphamvu ndi ochuluka komanso ataliatali ngati
Aanaki amakhala kumeneko. 11 Ngati Aanaki, nawonso ankawayesa kuti
anali Arefai, koma Amowabu ankawatcha iwo Aemi. 12 Ahori amakhala
ku Seiri koma adzukulu a Esau anawapirikitsa. Iwo anawononga
Ahori pamaso pawo nawakhalira pamalo pawo monga Aisraeli anachitira
m’dziko limene Yehova anawapatsa ngati chuma chawo).

13 Ndipo Yehova anati, “Tsopano nyamukani ndipo muwoloke Chigwa
cha Zeredi.” Choncho tinawoloka chigwacho.

14 Panapita zaka 38 kuchokera pa nthawi imene tinachoka ku Kadesi
Barinea mpaka pamene tinawoloka Chigwa cha Zeredi. Pa nthawi imeneyi
n’kuti m’bado wonse wa anthu ankhondowo utawonongeka ku msasa

monga Yehova anawalumbirira. 15 Dzanja la Yehova linatsutsana nawo
mpaka wonse anathera ku msasa.

16 Tsono atafa munthu wotsiriza mwa anthu ankhondowo, 17 Yehova
anati kwa ine, 18 “Lero mudutsa malire a Mowabu ku Ari podzera ku
Ari. 19 Mukafika kwa Aamoni, musawavutitse kapena kuwaputa, popeza
sindidzakupatsani gawo lililonse la dziko la Aamoni. Ine ndalipereka
dzikoli ngati chuma kwa adzukulu a Loti.”

20 (Ilinso ankaliyesa dziko la Arefai amene ankakhala kumeneko. Koma
Aamoni ankawatcha iwo Azamuzumi. 21 Iwo anali anthu amphamvu
ndiponso ochuluka, ataliatali ngati Aanaki. Yehova anawawononga ndi
kuwachotsa pamaso pa Aamoni, amene anawapirikitsa nawakhalira pa
malo pawo. 22 Yehova anachitanso chimodzimodzi ndi adzukulu a Esau
omwe anakhazikika ku Seiri atawononga Ahori powachotsa pamaso
pawo. Iwo anawapirikitsa Ahoriwo ndi kuwakhalira pamalo pawo mpaka
lero. 23 Ndipo za Aavi omwe ankakhala m’midzi yofika mpaka ku Gaza,
anagonjetsedwa ndi Akafitori wochokera ku Akafitori nakhala pamalo
pawo).

### *Kugonjetsedwa kwa Sihoni Mfumu ya ku Hesiboni*

24 “Tsopano nyamukani, muwoloke khwawa la Arinoni. Taona
ndapereka m’manja mwako Sihoni Mwamori mfumu ya Hesiboni ndi
dziko lake lonse. Yambapo kutenga chuma chake ndi kumenyana naye
nkhondo. 25 Lero lomwe lino ndidzayamba kuyika chiopsezo ndi mantha
pa mitundu yonse pansi pa thambo kuti akuope. Iwowo adzamva zambiri
yako ndipo adzanjenjemera ndi kuwawidwa mtima chifukwa cha iwe.”

26 Ine ndinatuma amithenga kuchokera ku chipululu cha Kedemoti
kupita kwa Sihoni mfumu ya Hesiboni kukanena mawu ofuna mtendere
ndipo ndinati, 27 “Tiloleni tidutse m’dziko mwanu. Ife tidzangodutsa
ndi msewu waukulu, ndipo sitidzapatukira kumanja kapena kumanzere.
28 Mutigulitse chakudya kuti tidye ndi madzi kuti timwe pa mtengo
wa siliva. Mungotilola kuti tidutse, tikuyenda pansi 29 monga mmene
anatichitira adzukulu a Esau okhala ku Seiri ndi Amowabu okhala ku
Ari mpaka titawoloka Yorodani kufika ku dziko limene Yehova Mulungu
wathu akutipatsa.” 30 Koma Sihoni mfumu ya Hesiboni sanalole kuti
tidutse. Popeza Yehova Mulungu wanu analimbitsa mzimu wake, nawu-
mitsa mtima wake kuti amupereke m’manja mwanu monga wachitira lero
lino.

31 Yehova anati kwa ine, “Taona ndayamba kumupereka Sihoni ndi dziko
lake kwa iwe. Tsopano yamba kugonjetsa ndi kulanda dziko lake.”

32 Sihoni ndi ankhondo ake atabwera kudzakumana nafe mwankhondo
pa Yahazi, 33 Yehova Mulungu anamupereka iye kwa ife ndipo tinankan-
tha, pamodzi ndi ana ake aamuna ndi gulu lake lonse lankhondo.
34 Pa nthawi imeneyi tinamulanda mizinda yake yonse ndi kuyiwononga
kwathunthu, amuna, akazi ndi ana. Palibe amene anapulumuka. 35 Koma
ziweto ndi zinthu zonse zimene tinalanda m’mizinda imene tinagonjet-
sayo, tinazitenga kukhala zathu. 36 Kuchokera ku Aroeri m’mphepete
mwa mtsinje wa Arinoni ndi ku mzinda wa ku mtsinjeko mpaka kukafika
ku Giliyadi, panalibe ndi mzinda ndi umodzi omwe umene unatikanika
kuwugonjetsa. Yehova Mulungu wathu anatipatsa onsewo. 37 Molingana
ndi lamulo la Yehova Mulungu wathu, simunalowerere dziko lililonse
la Aamoni, ngakhale dera lonse la ku mtsinje wa Yaboki kapena dera
lozungulira dera la ku mizinda ya ku mapiri.

# 3

*Kugonjetsedwa kwa Ogi Mfumu ya ku Basani*

1 Kenaka tinakhota ndi kumayenda mokwera mtunda ndi njira yolowera
ku Basani. Ndipo Ogi mfumu ya ku Basani ndi gulu lake lonse lankhondo
anakumana nafe ndipo anamenyana nafe ku Ederi. 2 Yehova anati
kwa ine, "Usachite naye mantha pakuti ndamupereka m'manja mwako
pamodzi ndi gulu lake lonse lankhondo ndi dziko lake lomwe. Ndipo
uchite kwa iye zimene unachita Sihoni mfumu ya Aamori, amene
ankalamulira ku Hesiboni."
3 Choncho Yehova Mulungu wathu anapereka m'manja mwathu Ogi
mfumu ya ku Basani ndi gulu lake lonse lankhondo. Tinawakantha
onsewo osasiya ndi mmodzi yemwe. 4 Pa nthawi imeneyo tinatenga
mizinda yake yonse. Pa mizinda 60, panalibe ndi umodzi womwe umene
sitinawalande, m'dera lonse la ufumu wa Ogi ku Basani chimene ndi
chigawo cha Arigobu. 5 Mizinda yonseyi inali yotetezedwa ndi malinga
ataliatali wokhala ndi zitseko ndi zitsulo, komabe panali midzi ina yambiri
imene inalibe malinga. 6 Tinawawonongeratu monga momwe tinachitira
Sihoni, mfumu ya ku Hesiboni. Tinawononga mzinda uliwonse, amayi,
amuna ndi ana omwe. 7 Koma tinafunkha ziweto ndi katundu wawo
yense.
8 Choncho pa nthawi imeneyi tinalanda kwa mafumu awiri Aamori, dera
la kummawa kwa Yorodani, kuyambira ku khwawa la Arinoni mpaka ku
Phiri la Herimoni. 9 (Asidoni amatcha Herimoni kuti Siriyoni, pamene
Aamori amalitcha Seniri). 10 Tinalanda mizinda yonse ya ku mapiri, ku
Giliyadi, Basani mpaka ku Saleka ndi Ederi, mizinda ya mu ufumu wa Ogi
wa ku Basani. 11 (Ogi, mfumu ya ku Basani, anali yekhayo amene anatsala
mwa mtundu wa anthu ataliatali a Chirefai. Bedi lake linali lachitsulo
ndipo lalitali kuposa mamita anayi. Mulifupi mwake munali mamita awiri.
Bedilo likanalipo ku Raba kwa Aamori).

*Kugawana Dziko*

12 Dziko limene tinalanda nthawi imeneyo, ndinapatsa fuko la Rubeni
ndi fuko la Gadi dera la kumpoto kwa Aroeri cha m'mphepete mwa
khwawa la Arinoni kuphatikizapo theka la dziko lamapiri la Giliyadi
ndi mizinda yake. 13 Theka la fuko la Manase ndinalipatsa dziko lonse
lotsala la Giliyadi ndi Basani yense yemwe ndi dera la ufumu wa Ogi.
(Chigawo chonse cha Arigobu mu Basani chinkadziwika kuti ndi dziko
la Arefai. 14 Yairi, mdzukulu wa Manase, anatenga chigawo chonse cha
Arigobu mpaka ku malire a Agesuri ndi Amaakati. Anatcha chigawochi
dzina lake, moti mpaka lero Basani amatchedwa Havoti Yairi). 15 Ndipo
ndinapereka Giliyadi kwa Makiri. 16 Koma kwa fuko la Rubeni ndi
fuko la Gadi ndinapereka chigawo chochokera ku Giliyadi kutsetsereka
mpaka ku khwawa la Arinoni (pakati pa khwawalo ndiye panali malire)
ndi kupitirira mpaka ku mtsinje wa Yaboki umene ndi malire Aamoni.
17 Malire ake a chakumadzulo anali Yorodani ku Araba, kuchokera ku
Kinereti mpaka ku Nyanja ya Araba (Nyanja ya Mchere), m'munsi mwa
matsitso a Pisiga.
18 Ndinakulamulirani nthawi imene ija kuti, "Yehova Mulungu wanu
wakupatsani dziko ili kuti likhale lanu. Koma amuna amphamvu onse
ali ndi zida zankhondo, awoloke kutsogolera abale anu Aisraeli. 19 Koma
akazi anu, ana anu ndi ziweto zanu (ndikudziwa kuti muli ndi ziweto

zambiri) zikhoza kumakhalabe m'mizinda imene ndakupatsani, [20] mpaka
Yehova atapereka mpumulo kwa abale anu, nawonso atatenga dziko
limene Yehova Mulungu wanu akuwapatsa patsidya pa Yorodani, monga
wachitira ndi inu. Kenaka, aliyense wa inu akhoza kudzabwerera ku dziko
limene ndinakupatsani."

*Mose Aletsedwa Kuwoloka Yorodani*

[21] Nthawi imeneyo ndinamulamula Yoswa kuti, "Waona wekha ndi maso
ako zonse zimene Yehova Mulungu wako anachitira mafumu awiriwa.
Yehova adzachita zomwezo ndi mafumu ena onse kumene mukupi-
tako. [22] Musawaope chifukwa Yehova Mulungu mwini adzakumenyerani
nkhondo."

[23] Nthawi imeneyo ndinachonderera Yehova kuti, [24] "Ambuye Mulungu,
mwayamba tsopano kuonetsa mtumiki wanu ukulu wanu ndi dzanja lanu
lamphamvu. Ndi mulungu uti ali kumwamba kapena pa dziko lapansi
amene angachite ntchito zozizwitsa zimene mumachita? [25] Mundilole
ndipite ndi kukaona dziko labwinolo kutsidya kwa Yorodani dziko la
mapiri abwinowo ndi Lebanoni."

[26] Koma chifukwa cha inu, Yehova anakwiya nane osandimvera.
Yehova anati, "Basi pakwana, usayankhulenso ndi ine zimenezi. [27] Pita
pamwamba pa phiri la Pisiga ndipo uyang'ane kumadzulo, kumpoto,
kummwera ndi kummawa. Ulione dzikolo ndi maso ako pakuti su-
woloka Yorodaniyu. [28] Koma langiza Yoswa ndipo umulimbikitse ndi
kumupatsa mphamvu pakuti adzatsogolera anthu awa kuwoloka ndipo
adzawathandiza kuti atenge dziko limene ulioneli." [29] Ndipo tinakhala
m'chigwa pafupi ndi Beti-Peori.

# 4

*Alamulidwa Kukhala Womvera*

[1] Mverani inu Aisraeli, malangizo ndi malamulo amene ndikuphun-
zitseni. Muwatsatire kuti mukhale ndi moyo ndi kuti mulowe ndi
kutenga dziko limene Yehova Mulungu wa makolo anu akukupatsani.
[2] Musawonjezere pa zimene ndikukulamulirani ndipo musachotserepo,
koma muwasunge malamulo a Yehova Mulungu wanu amene ndikuku-
patsani.

[3] Inu munaona ndi maso anu zimene Yehova anachita ku Baala-Peori.
Yehova Mulungu wanu anawononga aliyense amene anatsata Baala wa
ku Peori pakati panu. [4] Koma inu nonse amene munagwiritsitsa Yehova
Mulungu wanu mukanali ndi moyo mpaka lero.

[5] Taonani, ndakuphunzitsani malangizo ndi malamulo monga Yehova
Mulungu wanga anandilamulira kuti inuyo muwatsatire m'dziko limene
mukulowa ndi kulitengali. [6] Muwasunge mosamalitsa pakuti zimenezi
zidzaonetsa nzeru zanu ndi kuzindikira kwanu kwa anthu a mitundu ina,
amene adzamva za malangizo onsewa nati, "Ndithudi, mtundu waukulu
uwu ndi wa anthu anzeru ndi ozindikira." [7] Mtundu wina wa anthu ndi
uti umene uli waukulu chomwechi, woti ukhoza kukhala ndi milungu
yawo pafupi monga mmene alili Yehova Mulungu wathu ndi ife nthawi
zonse pamene tipemphera kwa Iye? [8] Ndipo ndi mtundu uti mwa mitundu
ya anthu umene ndi waukulu chotere kuti n'kukhala ndi malangizo ndi
malamulo olungama ngati malamulo amene ndikuyika pamaso panu lero?

[9] Inu mungosamala ndi kudziyang'anira kwambiri nokha kuti musayi-
wale zimene maso anu aona. Musalole kuti zichoke m'mitima mwanu

pa moyo wanu wonse. Zimenezi muziphunzitse kwa ana anu ndi
zidzukulu zanu ngakhale m'tsogolo. 10 Kumbukirani tsiku limene
munayimirira pamaso pa Yehova Mulungu wanu ku Horebu, pamene
anati kwa ine, "Sonkhanitsa anthu pamaso panga kuti amve mawu
anga ndi kuti aphunzire kundilemekeza m'moyo wawo onse m'dzikomo
ndi kuti ana awo aziwaphunzitsa zimenezi." 11 Munabwera pafupi
ndi kuyima pa tsinde pa phiri pamene phirilo limayaka moto umene
umafika mpaka kumwamba. Panalinso mtambo wakuda ndi mdima
wambiri. 12 Kenaka Yehova anayankhula nanu kuchokera m'motowo.
Inu munamva mawu ake okha koma simunamuone pakuti panali mawu
chabe. 13 Iye anakuwuzani Malamulo Khumi omwe ndi pangano lake
limene anakulamulirani kuti mutsatire. Ndipo anawalemba malamulowo
pa mapale awiri a miyala. 14 Ndipo Yehova anandilamula nthawi imene ija
kuti ndikuphunzitseni malangizo ndi malamulo amene muyenera kutsata
m'dziko limene mutenge mukawoloka Yorodani.

### *Mafano Aletsedwa*

15 Tsiku limene Yehova anayankhula nanu ku Horebu m'moto uja,
simunaone thupi lake. Choncho mudziyang'anire nokha mosamalitsa,
16 kuti musasokonezeke ndi kudzipangira nokha fano kapena chifanizo
cha mtundu uliwonse, kaya chokhala ngati mwamuna kapena ngati
mkazi, 17 kaya chokhala ngati nyama iliyonse ya pa dziko lapansi kapena
mbalame iliyonse yowuluka mlengalenga. 18 Kapena cholengedwa chili-
chonse choyenda pa nthaka kapena nsomba ya m'madzi akuya. 19 Ndipo
pamene muyang'ana kumwamba muona dzuwa, mwezi ndi nyenyezi,
zonse zakumwambazo musakopeke kuti muzigwadire ndi kumapembedza
zinthu zimene Yehova wapereka kwa anthu a mitundu yonse pa dziko
lapansi. 20 Koma inuyo, Yehova anakutengani ndi kukutulutsani m'ng'anjo
yosungunulira zitsulo, ku Igupto kuti mukhale anthu olandira chuma
chake monga mmene mulili tsopano.

21 Yehova anakwiya nane chifukwa cha inu, ndipo analumbira
kwathunthu kuti sindidzawoloka Yorodani ndi kulowa m'dziko labwinolo
limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani inu ngati cholowa chanu.
22 Ine ndifera m'dziko lino, sindiwoloka Yorodani. Koma inu mwat-
sala pang'ono kuwoloka ndi kukatenga dziko labwinolo. 23 Samalani,
musayiwale pangano limene Yehova Mulungu wanu anapangana nanu
ndipo musadzipangire nokha fano la chinthu chilichonse chimene Yehova
Mulungu wanu waletsa. 24 Pakuti Yehova Mulungu wanu ndi moto
wonyeketsa ndipo ndi Mulungu wansanje.

25 Mukadzakhala nthawi yayitali m'dzikomo ndi kubereka ana ndi
kukhala ndi zidzukulu ndipo mukadzasokonekera ndi kupanga fano
la mtundu uliwonse, n'kumachita zoyipa pamaso pa Yehova Mulungu
wanu ndi kumukwiyitsa, 26 ine ndi kuti kumwamba ndi dziko la-
pansi zikhale mboni lero zokutsutsani kuti mudzawonongedwa msanga
ndipo mudzachotsedwa m'dziko limene mutenge mukawoloka Yorodani.
Simudzakhalitsa kumeneko koma mudzawonongedwa ndithu. 27 Yehova
adzakubalalitsani pakati pa anthu ena. Ochepa okha pakati panu ndi
amene adzapulumuke pakati pa anthu a mitundu ina kumene Yehova
adzakupirikitsireniko. 28 Kumeneko mudzapembedza milungu ya mitengo
ndi miyala yopangidwa ndi anthu, imene singaone kapena kumva kapena
kudya kapena kununkhiza. 29 Mukanali komweko, ngati mudzamufuna-
funa Yehova Mulungu wanu mudzamupeza koma ngati mutamufunafuna

ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse. 30 Mukadzakhala pa
chipsinjo ndipo zonsezi zikadzakuchitikirani, ndi pamene pambuyo pake
mudzabwerera kwa Yehova Mulungu wanu ndi kumumvera Iye. 31 Pakuti
Yehova Mulungu wanu ndi Mulungu wachifundo, Iye sadzakutayani
kapena kukuwonongani kapena kuyiwala pangano lake ndi makolo anu,
limene analitsimikiza mwa lumbiro.

### *Yehova Ndiye Mulungu*

32 Tsopano tafunsani za masiku a m'mbuyomu, zakale inu musan-
abadwe, kuyambira tsiku limene Mulungu analenga munthu pa dziko la-
pansi. Tafufuzani kuyambira kumapeto mpaka mapeto anzake a thambo.
Kodi chinachitikako china chachikulu ngati ichi, kapena chinayamba
chamvekako chokhala ngati ichi? 33 Kodi uliponso mtundu wina wa
anthu umene unamva mawu a Mulungu akuyankhula kuchokera m'moto
n'kukhala ndi moyo monga mwachitira inumu? 34 Kodi alipo mulungu
amene anayeserapo kudzitengera mtundu wa anthu kuwachotsa mu
mtundu unzake mwa mayesero, zizindikiro zozizwitsa, nkhondo, komanso
mwa mphamvu zake zopanda malire, kapena mwa zochita zazikulu ndi
zochititsa mantha, monga zimene Yehova Mulungu wanu anakuchitirani
ku Igupto inu mukupenya?

35 Iye anakuonetsani zonsezi kuti inu muzindikire kuti Yehova ndiye
Mulungu, palibenso wina wofanana naye. 36 Kuchokera kumwamba, Iye
anafuna kuti inu mumve mawu ake ndi kuti mukhale osunga mwambo.
Pa dziko lapansi anakuonetsani moto waukulu, ndipo inu munamva
mawu ake kuchokera m'motomo. 37 Popeza anakonda makolo anu ndi
kusankha adzukulu awo, a pambuyo pawo, anakutulutsani kuchoka ku
Igupto ali pakati panu ndi mphamvu yake, 38 kuti akupirikitsireni mayiko
akuluakulu ndi amphamvu kuposa inu, ndi kukubweretsani inu ku dziko
lawo kuti likhale lanu, monga liliri lero.

39 Vomerezani lero ndipo dziwani mu mtima mwanu kuti Yehova ndiye
Mulungu kumwamba ndi pa dziko lapansi. Palibenso wina. 40 Sungani
malangizo ake ndi malamulo ake amene ndikukupatsani lero lino, kuti
zikuyendereni bwino inu ndi ana anu kutsogoloko, ndi kuti mukhalitse
m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani kwa nthawi zonse.

### *Mizinda Yothawirako*

41 Kenaka Mose anapatula mizinda itatu cha kummawa kwa Yorodani,
42 kumene aliyense amene wapha munthu akhoza kuthawirako ngati
wopha munthuyo sanaphe mnzakeyo mwadala ndi maganizo oyipa. Iye
akhoza kuthawira ku umodzi mwa mizinda imeneyi napulumutsa moyo
wake. 43 Mizindayo inali iyi: ku fuko la Rubeni, unali mzinda wa Bezeri
ku mapiri a ku chipululu; ku fuko la Gadi, unali Ramoti ku Giliyadi; ndipo
ku fuko la Manase, unali Golani ku Basani.

### *Kufotokozera za Malamulo*

44 Awa ndi malamulo amene Mose anapereka kwa Aisraeli. 45 Izi ndi
ndondomeko, malangizo ndi malamulo amene Mose anawapatsa iwo
pamene anatuluka ku Igupto. 46 Anali ku chigwa cha kufupi ndi Beti-
Peori mbali ya kummawa kwa Yorodani, m'dziko la Sihoni mfumu ya
Aamori amene ankalamulira ku Hesiboni ndipo anagonjetsedwa ndi Mose
ndi Aisraeli pamene ankachokera ku Igupto. 47 Iye anamulanda dziko
lake ndi dziko la Ogi mfumu ya ku Basani. Awa anali mafumu awiri
Aamori a kummawa kwa Yorodani. 48 Dziko ili linayambira ku Aroeri cha

kumphepete kwa khwawa la Arinoni ku phiri la Siyoni (limeneli ndi phiri
la Herimoni), 49 ndi kuphatikizapo dziko lonse la Araba cha kummawa
kwa Yorodani mpaka kukafika ku Nyanja ya Araba, kumunsi kwa Phiri la
Pisiga.

# 5

*Malamulo Khumi*

1 Mose anayitanitsa Aisraeli onse nati:
Tamverani inu Aisraeli, malangizo ndi malamulo amene ndikuwuzeni
lero. Muwaphunzire ndi kuonetsetsa kuti mukuwatsata. 2 Yehova
Mulungu wathu anachita pangano ndi ife ku Horebu. 3 Yehova sanachite
pangano ndi makolo athu koma ndi ife, tonse amene tili moyo lero.
4 Yehova anayankhula nanu maso ndi maso kuchokera m'moto pa phiri
paja. 5 (Pa nthawi imeneyo ine ndinayimirira pakati pa Yehova ndi inu
kuti ndikuwuzeni mawu a Yehova, chifukwa inu munkachita mantha ndi
moto ndipo simunakwere ku phiri). Ndipo Iye anati:

6 "Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakutulutsa ku
Igupto, m'dziko la ukapolo.

7 "Usakhale ndi milungu ina koma Ine ndekha.

8 "Usadzipangire chofanizira chinthu chilichonse chakumwamba
kapena cha pa dziko lapansi kapena cha m'madzi a pansi pa dziko.
9 Usazigwadire kapena kuzipembedza, pakuti Ine Yehova Mulungu
wako, ndine Mulungu wansanje, wolanga ana chifukwa cha tchimo la
makolo awo mpaka m'bado wachitatu ndi wachinayi wa iwo amene
amadana nane, 10 koma ndimaonetsa chikondi chosasinthika ku
mibado miyandamiyanda ya anthu amene amandikonda ndi kusunga
malamulo anga.

11 "Usagwiritse ntchito molakwika dzina la Yehova Mulungu wako,
pakuti Yehova adzamutenga kukhala wochimwa aliyense amene
akugwiritsa ntchito dzina lakelo molakwika.

12 "Uzisunga tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika monga momwe
Yehova Mulungu wako anakulamulira. 13 Uzigwira ntchito zako
zonse masiku asanu ndi limodzi, 14 koma tsiku lachisanu ndi chiwiri
ndi Sabata, tsiku loperekedwa kwa Yehova Mulungu wako. Tsiku
limeneli musagwire ntchito iliyonse, inuyo kapena mwana wanu
wamwamuna kapena mwana wanu wamkazi kapena wantchito
wanu wamwamuna kapena mdzakazi wanu kapena ng'ombe yanu
kapena bulu wanu kapena ziweto zanu kapena mlendo amene
akukhala m'mudzi mwanu, motero ndiye kuti wantchito wanu
wamwamuna ndi wantchito wanu wamkazi adzapumula monga
inuyo. 15 Kumbukira kuti unali kapolo ku Igupto ndipo Yehova
Mulungu wako anakutulutsa kumeneko ndi dzanja lamphamvu ndi
lotambasuka. Choncho Yehova Mulungu wako akukulamula kuti
uzisunga tsiku la Sabata.

16 "Lemekeza abambo ako ndi amayi ako monga Yehova Mulungu wako
wakulamulira iwe kuti ukhale ndi moyo wautali ndi kuti zikuyendere
bwino m'dziko limene Yehova Mulungu wako akukupatsa.

17 "Usaphe.

18 "Usachite chigololo.

19 "Usabe.

20 “Usapereke umboni womunamizira mnzako.
21 “Usasirire mkazi wa mnzako. Usasirire nyumba ya mnzako kapena
munda wake, wantchito wake wamwamuna kapena mdzakazi wake,
ng’ombe yake kapena bulu wake, kapena chilichonse cha mnzako.”

22 Awa ndi malamulo amene Yehova anayankhula ndi mawu okweza
kwa gulu lanu lonse pa phiri paja m’moto, mtambo ndi mdima woopsa,
sanawonjezerepo kanthu. Ndipo anawalemba pa mapale awiri amiyala
ndi kundipatsa.

23 Mutamva mawu kuchokera mu mdimawo, phiri lili moto lawilawi,
atsogoleri onse a mafuko anu ndi akuluakulu anu anabwera kwa ine.
24 Ndipo munati, “Yehova Mulungu wathu wationetsa ulemerero ndi ukulu
wake, ndipo tamva mawu ake kuchokera m’moto. Lero taona kuti munthu
akhoza kukhala ndi moyo ngakhale Mulungu atayankhula naye. 25 Koma
tsopano tife chifukwa chiyani? Moto waukuluwu utinyeketsa, ndipo tifa
tikapitirirabe kumva mawu a Yehova Mulungu wathu. 26 Pakuti ndi
munthu uti wolengedwa amene anamvapo mawu a Mulungu wamoyo
akuyankhula kuchokera m’moto, monga tachitiramu, nakhala ndi moyo?
27 Pita pafupi kuti ukamvetsere zonse zimene Yehova Mulungu wathu
akunena. Kenaka udzatiwuze chilichonse chimene Yehova Mulungu
wathu akunena ndipo tidzamvera ndi kuchita.”

28 Yehova anakumvani pamene munkayankhula kwa ine ndipo Yehova
anati kwa ine, “Ndamva zimene anthuwa anena kwa iwe. Chilichonse
chimene anena ndi chabwino. 29 Zikanakhala bwino akanakhala ndi
mtima wondiopa ndi kusunga malamulo anga nthawi zonse kuti zinthu
ziziwayendera bwino, iwowo pamodzi ndi ana awo kwamuyaya.

30 “Pita uwawuze kuti abwerere ku matenti awo. 31 Koma iwe ukhale
kuno ndi ine kuti ndikupatse malamulo, malangizo ndi ziphunzitso zimene
azitsatira m’dziko limene ndiwapatse kuti alitenge.”

32 Choncho samalirani kuchita zimene Yehova Mulungu wanu akuku-
lamulirani inu, musapatukire kudzanja lamanja kapena lamanzere.
33 Muyende m’njira yonse imene Yehova Mulungu wanu wakulamulirani
kuti mukhale ndi moyo ndi kupambana, ndi kuti masiku anu achuluke
m’dziko limene mudzatengelo.

# 6

### *Konda Yehova Mulungu Wako*

1 Awa ndi malamulo, malangizo ndi ziphunzitso zimene Yehova Mu-
lungu wanu anandilamula kuti ndikuphunzitseni kuti mukawatsatire
m’dziko limene mukuwolokera Yorodani kuti mukalitenge, 2 kuti inuyo,
ana anu, ndi zidzukulu zanu m’tsogolomo mudzaope Yehova Mulungu
wanu moyo wanu wonse posunga malangizo ndi malamulo ake onse
amene ndinakupatsani inu kuti musangalale ndi moyo wautali. 3 Mvera
Israeli ndipo usamalitse kuchita malamulowa kuti zinthu zikuyendere
bwino m’dziko ndi kuti muchuluke kwambiri m’dziko loyenda mkaka ndi
uchi monga momwe Yehova Mulungu wa makolo anu anakulonjezerani.

4 Tamvani inu Aisraeli, Yehova Mulungu wathu, Yehova ndi mmodzi.
5 Uzikonda Yehova Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako
wonse, ndi mphamvu zako zonse. 6 Malamulo amene ndakupatsani lero
ayenera kukhala mu mtima mwanu. 7 Muziwaphunzitsa mwachangu kwa
ana anu. Muzikamba za malamulowa pamene muli m’nyumba zanu,

pamene mukuyenda m'njira, pamene mukugona ndi pamene mukudzuka.
8 Muwamange ngati zizindikiro pa manja anu ndi kuwamangirira pa
zipumi zanu. 9 Muwalembe pa mphuthu za nyumba zanu ndi pa zipata
zanu.

10 Pamene Yehova Mulungu wanu akukulowetsani ndi kukupatsani
dziko limene analumbirira makolo anu Abrahamu, Isake ndi Yakobo,
dziko lokhala ndi mizinda ikuluikulu imene inu simunamange, 11 nyumba
zodzaza ndi zinthu za mitundu yonse zimene inu simunayikemo, zit-
sime zimene inu simunakumbe, minda ya mpesa ndi mitengo ya olivi
zimene inuyo simunadzale, tsono mukadya ndi kukhuta, 12 samalani kuti
mungayiwale Yehova amene anakutulutsani ku Igupto, kukuchotsani mu
ukapolo.

13 Muziopa Yehova Mulungu wanu ndi kumutumikira Iye yekha, ndipo
muzilumbira pa dzina lake. 14 Musamatsatire milungu ina, milungu ya
anthu ena okuzungulirani, 15 pakuti Yehova Mulungu wanu amene ali
pakati panu, ndi Mulungu wansanje ndipo adzakukwiyirani kwambiri
ndi kukuwonongani, kukufafanizani m'dziko. 16 Musamuyese Yehova Mu-
lungu wanu monga munachitira ku Masa. 17 Onetsetsani kuti mukusunga
malamulo a Yehova Mulungu wanu, malangizo ake ndi zikhazikitso
zake zimene anakulamulirani. 18 Chitani zoyenera ndi zabwino pamaso
pa Yehova, kuti zikuyendereni bwino ndi kuti mukhoza kukalowa ndi
kulanda dziko labwinolo limene Yehova analonjeza molumbira kwa
makolo anu, 19 kupirikitsiratu adani anu onse, monga Yehova wanenera.

20 M'tsogolo muno, ana anu akadzakufunsani kuti, "Kodi tanthauzo
la ndondomeko, malangizo, zikhazikitso ndi malamulo amene Yehova
Mulungu wathu anakulamulani n'chiyani?" 21 Inu mudzawawuze kuti,
"Ife tinali akapolo a Farao ku Igupto, koma Yehova anatitulutsa ku Igupto
ndi dzanja lamphamvu. 22 Ifeyo tikuona Yehova anatumiza zizindikiro
zozizwitsa ndi zodabwitsa, zazikulu ndi zoopsa, pa Aigupto ndi Farao
pamodzi ndi banja lake lonse. 23 Koma anatitulutsa kumeneko ndi
kutilowetsa kuno natipatsa dziko limene analonjeza mwa lumbiro kwa
makolo athu. 24 Yehova anatilamula kuti tizimvera malamulo onsewa, kuti
tizimuopa kuti zinthu zizitiyendera bwino pa moyo wathu monga momwe
zilili leromu. 25 Ndipo ngati tisamala kumvera malamulo onsewa pamaso
pa Yehova Mulungu wathu monga momwe anatilamulira ife, chimenecho
chidzakhala chilungamo chathu."

## 7

*Apirikitsa Mitundu Ina ya Anthu*

1 Pamene Yehova Mulungu wanu wakufikitsani m'dziko limene
mukukalowa ndi kulilanda ndi kuthamangitsa pamaso panu mitundu ya
anthu iyi: Ahiti, Agirigasi, Aamori, Akanaani, Aperezi, Ahivi ndi Ayebusi;
yomwe ndi mitundu isanu ndi iwiri yayikulu ndi yamphamvu kuposa
inu; 2 Yehova Mulungu wanu akadzawapereka m'manja mwanu, ndipo
inu mukadzawagonjetsa, mudzawawononge kwathunthu. Musadza-
chite mgwirizano ndi anthuwo ndiponso musadzawachitire chifundo.
3 Musadzakwatirane nawo. Musadzapereke ana anu aakazi kwa ana awo
aamuna kapena kutenga ana anu aamuna ndi kuwapereka kwa ana awo
aakazi. 4 Mukadzatero, iwo adzasocheretsa ana anu aamuna kuti asan-
ditsatire ndi kutumikira milungu ina. Motero Yehova adzakukwiyirani
ndi kukuwonongani mwachangu. 5 Koma mukachite izi: Mukagumule

maguwa awo ansembe, mukaswe miyala yawo yachipembedzo, mukadule
mitengo yawo ya Asera, ndi kutentha mafano awo pa moto. 6 Pakuti
inu ndinu anthu opatulika kwa Yehova Mulungu wanu. Yehova Mulungu
wanu anakusankhani pakati pa anthu onse pa dziko lapansi kuti mukhale
ake, chuma chake cha mtengo wapatali.

7 Yehova sanakukondeni chifukwa choti munali ochuluka kuposa ena
pakuti inuyo ndiye munali ochepetsetsa mwa anthu onse. 8 Koma
chifukwa chakuti Yehova anakukondani nasunga lumbiro lake limene
analumbira kwa makolo anu. Ndi chifukwa chake anakutulutsani
ndi mphamvu yake yopanda malire ndi kukupulumutsani ku dziko la
ukapolo, kuchoka m'manja mwa Farao mfumu ya ku Igupto. 9 Choncho
dziwani kuti Yehova Mulungu wanu, ndi Mulungu. Iye ndi Mulungu
wokhulupirika, wosunga pangano lake la chikondi chosasinthika ku
mibadomibado, kwa iwo amene amamukonda nasunga malamulo ake.
10 Koma

iwo amene amamuda adzawabwezera powawononga pamaso pawo;
sadzachedwa kuwabwezera iwo amene amadana naye.

11 Choncho muziyesetsa kusunga malamulo, malangizo ndi maphunziro
amene ndikukulamulani lero lino kuti muchite.

12 Mukamvera malamulo amenewa, ndi kusamala kuwatsata, ndiye kuti
Yehova Mulungu wanu adzasunga pangano lake la chikondi chosasinthika
ndi inu, monga analumbira kwa makolo anu. 13 Iye adzakukondani
nakudalitsani ndi kukuchulukitsani. Adzadalitsa chipatso cha m'mimba
mwanu, zokolola za m'dziko mwanu, tirigu wanu, vinyo wanu ndi
mafuta anu, ana ang'ombe zanu ndi ana ankhosa zanu m'dziko limene
analumbirira kwa makolo anu kuti akupatseni inu. 14 Inu mudzadalitsika
kuposa mtundu wina uliwonse wa anthu ndipo palibe mwamuna kapena
mkazi aliyense pakati panu amene adzakhale wosabereka. Ziweto zanu
nazonso, sipadzapezeka zosabereka. 15 Yehova adzakupewetsani ku ma-
tenda aliwonse. Sadzakugwetserani matenda owopsa aja munawadziwa
ku Igupto, koma adzawagwetsera pa odana nanu. 16 Muwononge anthu
onse amene Yehova Mulungu wanu awapereka kwa inu. Musawamvere
chisoni ndipo musatumikire milungu yawo pakuti umenewo udzakhala
msampha kwa inu.

17 Mukhoza kunena kuti, "Anthu awa ndi amphamvu kuposa ifeyo.
Nanga tingawapirikitse bwanji?" 18 Koma musachite nawo mantha,
kumbukirani bwino zimene Yehova Mulungu wanu anachita ndi Farao
pamodzi ndi Igupto yense. 19 Munadzionera nokha ndi maso anu
mayesero aakulu, zizindikiro zozizwitsa ndi zodabwitsa, mphamvu yake
yopanda malire imene Yehova Mulungu wanu anakutulutsirani. Yehova
Mulungu adzachita zimenezo ndi anthu onse amene muwaopa tsopano.
20 Kuwonjezera apo, Yehova Mulungu wanu adzatumiza mavu pakati
pawo mpaka atamaliza onse amene adzakubisalirani. 21 Musaopsedwe
nawo pakuti Yehova Mulungu wanu, amene ali pakati panu, ndi Mulungu
wamkulu ndi woopsa. 22 Yehova Mulungu wanu adzapirikitsa anthu
a mitundu yonse pamaso panu, pang'onopang'ono. Sadzakulolani
kuti muwathe nthawi imodzi, kuti nyama zakuthengo zingadzaswane
mokuzungulirani. 23 Koma Yehova Mulungu wanu adzawapereka kwa inu,
adzawasokoneza kufikira atawonongedwa. 24 Iye adzapereka mafumu
awo m'dzanja lanu, ndipo adzafafaniza mayina awo pa dziko lapansi.
Palibe amene adzalimbana nanu, inu mudzawawononga. 25 Muwawotche

pa moto mafano a milungu yawo. Musasirire siliva ndi golide amene ali pa mafanoyo. Musamutenge kuti akhale wanu chifukwa mukatero mudzakodwa naye ngati msampha, pakuti Yehova Mulungu wanu amanyansidwa
nazo. [26] Musabweretse chinthu chonyansa m'nyumba mwanu kuopa kuwonongedwa ngati chonyasacho. Muziyipidwa ndi kunyansidwa nacho kwambiri pakuti chidzawononongedwanso.

# 8

*Musayiwale Yehova*

[1] Samalani potsata lamulo lililonse limene ndikukupatsani lero, kuti mukhale ndi moyo ndi kuchulukana kuti mulande ndi kulowa m'dziko limene Yehova analumbira kuti adzapereka kwa makolo anu.
[2] Kumbukirani mmene Yehova Mulungu wanu anakutsogolerani njira yonse m'chipululu kwa zaka makumi anayi, kukutsitsani ndi kukuyesani kuti adziwe chimene chinali mu mtima mwanu ngati mungathe kusunga
malamulo ake kapena ayi. [3] Iye anakutsitsani nakumvetsani njala kenaka n'kukudyetsani mana amene anali osadziwika kwa inu kapena makolo anu, kuti akuphunzitseni kuti munthu sadzakhala ndi moyo ndi chakudya chokha koma ndi mawu aliwonse ochokera m'kamwa mwa Yehova.
[4] M'zaka makumi anayi zimenezi, zovala zanu sizinang'ambike ndipo
mapazi anu sanatupe. [5] Tsono dziwani mu mtima mwanu kuti monga abambo amalanga mwana wawo, momwemonso Yehova Mulungu wanu amakulangani.

[6] Samalirani malamulo a Yehova Mulungu wanu, kuyenda m'njira yake
ndi kumuopa Iye. [7] Pakuti Yehova Mulungu wanu akukulowetsani m'dziko labwino, dziko lokhala ndi mitsinje ndi mathawale a madzi, akasupe
oyenderera mu zigwa ndi m'mapiri, [8] dziko lokhala ndi tirigu ndi barele, mpesa ndi mitengo ya mkuyu, makangadza, mafuta a olivi ndi uchi;
[9] dziko limene buledi sadzasowa ndipo simudzasowa chilichonse; dziko limene miyala yake ndi chitsulo ndipo ku mapiri ake mukhoza kukumbako mkuwa.

[10] Mukadya ndi kukhuta, yamikani Yehova Mulungu wanu chifukwa
cha dziko labwino limene wakupatsani. [11] Samalani kuopa kuti mungayiwale Yehova Mulungu wanu posasunga malamulo, zikhazikitso ndi
malangizo ake amene ndikukupatsani lero, [12] kuopa kuti mukadya ndi
kukhuta, mukamanga nyumba zabwino ndi kukhalamo, [13] ndi pamene ng'ombe zanu ndi nkhosa zanu zaswana, ndi siliva ndi golide wanu
wachuluka ndiponso kuti zonse zimene muli nazo zachuluka, [14] mtima wanu udzayamba kunyada ndi kuyiwala Yehova Mulungu wanu, amene
anakutulutsani ku Igupto, kukuchotsani ku dziko la ukapolo. [15] Iye anakutsogolerani kudutsa m'chipululu chachikulu ndi chochititsa mantha, dziko lija la ludzu ndi lopanda madzi, lokhala ndi njoka zaululu ndi
zinkhanira. Iye anatulutsa madzi kuchokera m'thanthwe lowuma. [16] Iye anakupatsani mana kuti mudye m'chipululu, zinthu zoti ngakhale makolo anu sanazidziwe, kuti akuchepetseni ndi kukuyesani ndipo kuti pa mapeto
pake zikuyendereni bwino. [17] Mu mtima mwanu mukhoza kuganiza kuti, "Mphamvu zanga ndi kulimbika kwa dzanja langa ndi zimene zandile-
meretsa chonchi." [18] Koma kumbukirani Yehova Mulungu chifukwa ndi amene amakupatsani mphamvu zopezera chuma chimenechi kuti atsimikize pangano limene analumbira kwa makolo anu, monga liliri lero lino.

19 Ine ndine mboni yokutsutsani lero lino, kuti mukayiwala Yehova Mu-
lungu wanu ndi kutsata milungu ina n’kumayigwadira, mudzawonongeka
ndithu. 20 Monga mitundu ina ya anthu imene Yehova anayiwononga
pamaso panu, inunso mudzawonongedwa chifukwa chosamvera Yehova
Mulungu wanu.

# 9

*Osati Chifukwa cha Kulungama kwa Israeli*

1 Mvera Israeli. Watsala pang’ono kuwoloka Yorodani ndi kukathaman-
gitsa mitundu ikuluikulu ndi yamphamvu kuposa iweyo, imene mizinda
yake ndi ikuluikulu yokhala ndi makoma ofika mpaka kumwamba.
2 Anthuwo ndi ataliatali, Aanaki! Ukudziwa za iwo ndipo unamvapo
zikunenedwa kuti, “Ndani amene angalimbane ndi Aanaki?” 3 Koma
khulupirira lero kuti Yehova Mulungu wako amene ali patsogolo pako
ali ngati moto wonyeketsa. Adzawononga iwowo ndipo adzawag-
onjetsa iweyo ukuona. Pamenepo udzawathamangitsa ndi kuwakantha
mwamsanga, monga momwe Yehova wakulonjezera.

4 Yehova Mulungu wako akadzawapirikitsa pamaso pako, usadzanene
mu mtima mwako kuti, “Yehova wandibweretsa kuno kudzalanda dziko
lino chifukwa cha kulungama kwanga.” Ayi, koma ndi chifukwa
cha kuyipa kwa anthu amene Yehova ati awapirikitse pamaso pako.
5 Sukalowa ndi kutenga dziko lawolo chifukwa cha kulungama kwako
kapena kukhulupirika kwako koma chifukwa cha kuyipa kwa anthuwo.
Yehova Mulungu wako awapirikitsa pamaso pako kuti akwaniritse zimene
analumbira kwa makolo ako Abrahamu, Isake ndi Yakobo. 6 Tsono
zindikira kuti si chifukwa cha kulungama kwako kuti Yehova Mulungu
wako akukupatsa dziko labwinoli kuti ulitenge popeza ndiwe wokanika.

*Mwana Wang’ombe Wagolide*

7 Kumbukirani izi ndipo musayiwale mmene munaputira mkwiyo wa
Yehova Mulungu m’chipululu muja. Kuyambira tsiku limene munatuluka
mu Igupto mpaka pamene munafika kuno, mwakhala owukira Yehova.
8 Ku Horebu munaputa mkwiyo wa Yehova, kotero kuti anakwiya
kwambiri nafuna kukuwonongani. 9 Nditakwera ku phiri kuti ndika-
landire miyala iwiri ya malamulo, ya pangano limene Yehova anachita ndi
inu, ndinakhala ku phiriko kwa masiku makumi anayi usiku ndi usana,
sindinadye buledi kapena kumwa madzi. 10 Yehova anandipatsa miyala
iwiri yolembedwa ndi chala chake. Pa miyalapo panali malamulo onse
amene Yehova analengeza kwa inu pa phiri kuchokera m’moto pa tsiku la
msonkhano.

11 Pakutha pa masiku makumi anayi usiku ndi usana, Yehova anandi-
patsa miyala iwiri, miyala ya pangano. 12 Tsono Yehova anandiwuza,
“Tsikako kuno msanga, chifukwa anthu ako aja unawatulutsa ku Iguptowa
adziyipitsa. Iwo apatukapo mofulumira pa zimene ndinawalamulira
ndipo adzipangira fano lachitsulo.”

13 Ndipo Yehova anati kwa ine, “Anthu awa ndawaona ndipo ndi anthu
okanikadi! 14 Ndilekeni ndiwawononge ndi kufafaniza mayina awo pa
dziko lapansi. Ndipo ndidzakuyesa iwe mtundu wa anthu wamphamvu
ndi wochuluka kuposa iwo.”

15 Choncho ndinatembenuka ndi kutsika phiri moto ukanayakabe.
Ndipo miyala iwiri ya pangano inali m’manja mwanga. 16 Ine poyang’ana

ndinaona kuti inu munachimwira Yehova Mulungu wanu. Munadzipan-
gira fano lowumbidwa ngati mwana wang'ombe. Inuyo munapatuka
msanga kuchoka pa njira imene Yehova anakulamulirani. 17 Motero ine
ndinaponya pansi miyala imene inali m'manja mwanga, ndi kuyiphwanya
inu mukuona.

18 Tsono nthawi yomweyo ndinagwa chafufumimba pamaso pa Yehova
kwa masiku makumi anayi usiku ndi usana. Sindinadye buledi kapena
kumwa madzi chifukwa cha machimo onse amene munawachita, kuchita
zoyipa pamaso pa Yehova ndi kumukwiyitsa kwambiri. 19 Ine ndinachita
mantha ndi mkwiyo ndi ukali wa Yehova chifukwa anakwiya nanu
kokwanira kukuwonongani. Koma Yehova anandimveranso. 20 Ndipo
Yehova anakwiya ndi Aaroni ndipo akanamuwononga, koma ine ndi-
namupemphereranso Aaroniyo. 21 Ndiponso ndinatenga chinthu chanu
choyipacho, mwana wang'ombe amene munapangayo, ndi kumuwotcha
pa moto. Kenaka ndinamuphwanya ndi kumuperapera ndikukhala ngati
fumbi ndipo ndinawaza fumbilo mu mtsinje umene unkayenda kuchokera
m'phiri.

22 Inu munamukwiyitsanso Yehova ku Tabera, ku Masa ndi ku Kibiroti
Hatava.

23 Ndipo Yehova atakutulutsani ku Kadesi Barinea anati, "Pitani
mukatenge dziko limene ndakupatsani." Koma munawukira ulamuliro wa
Yehova Mulungu wanu. Inu simunamukhulupirire kapena kumumvera.
24 Kuyambira pamene ndinakudziwani, mwakhala owukira Yehova.

25 Ine ndinagwa chafufumimba pamaso pa Yehova kwa masiku makumi
anayi usana ndi usiku chifukwa Yehova ananena kuti akuwonongani.
26 Ndinapemphera kwa Ambuye ndi kuti, "Haa Yehova Wamkulukulu,
musawawononge anthu anu, chuma chanuchanu chimene munachip-
ulumutsa ndi mphamvu yanu yayikulu ku Igupto ndi dzanja lanu la
mphamvu. 27 Kumbukirani atumiki anu Abrahamu, Isake ndi Yakobo.
Musatengere kupulupudza, kuyipa ndi kuchimwa kwawo anthuwa.
28 Kupanda kutero, ndiye kuti anthu a ku dziko lija munatitulutsaku
adzati, 'Yehova anawatulutsa kuti akawaphe m'chipululu popeza sanathe
kukawalowetsa m'dziko limene anawalonjeza ndipo anadana nawo.'
29 Koma iwowa ndi anthu anu, chuma chanu chimene munachitulutsa ndi
mphamvu yanu yayikulu ndi mkono wanu wotambasuka."

# 10

### *Miyala Ngati Yoyamba Ija*

1 Pa nthawi imeneyo Yehova anati kwa ine, "Sema miyala iwiri yofanana
ndi yoyamba ija ndipo ubwere nayo kwa Ine ku phiri. Upangenso bokosi
lamatabwa. 2 Ndidzalembapo mawu amene anali pa miyala yoyamba
ija, imene unayiphwanya. Ndipo iwe ukuyenera kuyika miyalayo
m'bokosimo."

3 Choncho ndinapanga bokosi lamatabwa amtengo wa mkesha ndi
kusema miyala iwiri yofanana ndi yoyamba ija, ndipo ndinapita ku
phiri nditanyamula miyala iwiri m'manja mwanga. 4 Yehova analemba
pa miyala iwiriyo zimene analemba poyamba, Malamulo Khumi amene
analengeza kwa inu pa phiri paja, m'moto, pa tsiku la msonkhano. Ndipo
Yehova anawapereka kwa ine. 5 Tsono ndinatsika ku phiri kuja ndi kuyika
miyalayo m'bokosi ndinapanga lija monga Yehova anandilamulira, ndipo
panopa ili m'menemo.

6 Aisraeli anayenda kuchokera ku Beeroti Beni Yaakani mpaka ku
Mosera. Kumeneko Aaroni anamwalira nayikidwa m’manda, ndipo
mwana wake Eliezara anakhala wansembe m’malo mwake. 7 Kuchokera
kumeneko Aisraeli anapita ku Gudigoda, napitirira mpaka ku Yotibata, ku
dziko la mitsinje ya madzi. 8 Pa nthawi imeneyo Yehova anapatula fuko
la Levi kuti anyamule bokosi la pangano la Yehova lija, kuti ayimirire
pamaso pa Yehova, kutumikira ndi kunena madalitso pa dzina lake monga
amachitira mpaka lero. 9 N’chifukwa chake Alevi alibe gawo kapena
cholowa pakati pa abale awo. Yehova ndiye cholowa chawo monga
momwe Yehova Mulungu wanu anawawuzira.

10 Tsopano ndinakhala ku phiri kuja kwa masiku makumi anayi usana
ndi usiku monga ndinachitira poyamba, ndipo Yehova anandimveranso
nthawi iyi. Sichinali chifuniro chake kuti akuwonongeni. 11 Yehova anati
kwa ine, “Pita ndi kutsogolera anthuwa pa njira yawo, kuti alowe ndi
kulandira dziko limene ndinalumbira kwa makolo awo kuti ndiwapatse.”

*Kuopa Yehova*

12 Tsopano inu Aisraeli, n’chiyani chimene Yehova afuna kwa inu? Iye
akufuna kuti muzimuopa poyenda m’njira zake zonse ndi kumamukonda
Iye, kumutumikira Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse, ndi
moyo wanu wonse, 13 ndi kusunga malamulo ndi malangizo amene
ndikukupatsani lero kuti zizikuyenderani bwino.

14 Yehova Mulungu wanu ndiye mwini wake kumwamba ngakhale
mmwambamwamba, dziko lapansi ndi zonse zimene zili m’menemo.
15 Yehova anayika mtima wake pa makolo anu okha ndipo anawakondadi
nasankha adzukulu awo mwa mitundu yonse pa dziko lapansi, kunena
inuyo monga mulili lero. 16 Motero chitani mdulidwe wa mitima yanu
ndipo musakhalenso opulupudza. 17 Pakuti Yehova Mulungu wanu
ndi Mulungu wa milungu, Ambuye wa ambuye, Mulungu wamkulu,
wamphamvu ndi woopsa, amene sakondera ndipo salandira ziphuphu.
18 Iye amatchinjiriza ana amasiye ndi akazi amasiye, ndipo amakonda
mlendo namupatsa chakudya ndi chovala. 19 Muzikonda alendo popeza
inuyo munali alendo m’dziko la Igupto. 20 Muziopa Yehova Mulungu wanu
ndi kumutumikira Iye. Mumukakamire Iyeyo ndi kuchita malumbiro
anu m’dzina lake. 21 Iye ndiye matamando anu, Mulungu wanu amene
anakuchitirani zodabwitsa zazikulu ndi zoopsa zimene munaona ndi maso
anu zija. 22 Makolo anu amene anapita ku Igupto analipo makumi
asanu ndi awiri onse pamodzi, ndipo tsopano Yehova Mulungu wanu
wakuchulukitsani ngati nyenyezi zakumwamba.

# 11

*Kukonda ndi Kumvera Yehova*

1 Muzikonda Yehova Mulungu wanu ndipo nthawi zonse muzitsata
zimene Iyeyo anakulamulani, malangizo, zikhazikitso ndi malamulo ake.
2 Lero kumbukirani kuti si ana anu amene anaona ndi kulawa chilango
cha Yehova Mulungu wanu: ukulu wake, dzanja lake lamphamvu, mkono
wake wotambasuka; 3 zizindikiro zozizwitsa zimene anazionetsa ndi
zinthu zimene anazichita m’kati mwa Igupto, Farao mfumu ya Igupto
ndi kwa dziko lake lonse; 4 zimene Iye anachita kwa gulu lankhondo la
Aigupto, kwa akavalo ndi magaleta awo, mmene Iye anawamizira ndi
madzi a mu Nyanja Yofiira pamene amakuthamangitsani, ndi mmene

Yehova anawagonjetsera kufikira lero. 5 Si ana anu amene anaona
zimene Iye anakuchitirani m'chipululu kufikira pamene munafika pa malo
anu, 6 ndi zimene anachitira Datani ndi Abiramu, ana aamuna a Eliabu
mwana wa Rubeni, pamene nthaka inatsekula pakamwa pake pakati pa
Aisraeli onse ndi kuwameza pamodzi ndi katundu wawo, matenti awo
ndi chilichonse chawo. 7 Koma ndinuyo amene munaona ntchito zonse
zikuluzikulu zimenezi Yehova anakuchitirani.

8 Tsono muzisunga malamulo onse amene ndikukupatsani lero kuti
mukhale ndi mphamvu ndi kuti mupite kukalanda m'dziko limene
mwakhala pang'ono kulowamo mukawoloka Yorodani, 9 ndiponso kuti
mukhalitse m'dziko limene Yehova analumbira kupatsa makolo anu ndi
zidzukulu zawo, lomwe ndi dziko loyenda mkaka ndi uchi. 10 Dziko limene
mukukalanda ndi kulowamo silokhala ngati dziko la ku Igupto kumene
mukuchokera ayi, kuja mumadzala mbewu ndi kumathirira ndi mapazi
anu ngati ku dimba. 11 Koma dziko limene mukalande mukawoloka
Yorodani ndi dziko la mapiri ndi zigwa, dziko limene limalandira mvula
kuchokera kumwamba. 12 Ili ndi dziko limene Yehova Mulungu wanu
amalisamalira. Maso a Yehova Mulungu wanu amaliyang'anira nthawi
zonse kuchokera ku mayambiriro a chaka mpaka kumapeto kwake.

13 Choncho mukasunga mokhulupirika malamulo amene ndikukupat-
sani lero lino, kukonda Yehova Mulungu wanu ndi kumutumikira Iyeyo
ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse, 14 pamenepo ndidza-
tumiza mvula m'dziko mwanu pa nthawi yake m'nyengo ya dzinja ndi
chilimwe, kuti mudzakolole tirigu wambiri ndi kuti mudzakhale ndi vinyo
watsopano ndi mafuta. 15 Ndidzakupatsani udzu m'minda mwanu woti
muzidzadyetsera ng'ombe zanu ndipo inuyo mudzadya ndi kukhuta.

16 Dzisamalireni nokha, kuopa kuti mungakopeke mtima ndi kubw-
erera m'mbuyo kuyamba kutumikira milungu ina ndi kumayigwadira.
17 Mukatero Yehova Mulungu wanu adzakukwiyirani kwambiri, nadza-
letsa thambo kuti lisabweretsenso mvula ndipo dziko silidzapereka
zokolola. Choncho mudzawonongeka msanga m'dziko limene Yehova
akukupatsani. 18 Sungani mawu amenewa mu mtima mwanu ndi
m'maganizo mwanu, muwamangirire pa mikono yanu ndipo muwayike
pamphumi panu. 19 Mawuwa muziphunzitsa ana anu, muzikamba za iwo
pamene mukhala pansi m'nyumba zanu, pamene mukuyenda m'njira,
pamene mugona ndi pamene mukudzuka. 20 Muwalembe pa mphuthu
za nyumba zanu ndi pa zipata zanu, 21 kuti inu ndi ana anu mukhale
m'dziko limene Yehova analumbira kupatsa makolo anu mpaka kalekale
monga umakhalira mlengalenga pamwamba pa dziko.

22 Mukatsatira mosamalitsa malamulo amene ndikukupatsaniwa,
kukonda Yehova Mulungu wanu, kuyenda m'njira zake zonse ndi
kumugwiritsitsa Iye 23 Yehova adzapirikitsa mitundu ina yonseyi inu
musanafike ndipo mudzagonjetsa mitundu ikuluikulu ndi yamphamvu
kuposa inu. 24 Malo aliwonse amene mudzaponda adzakhala anu: dziko
lanu lidzachokera ku chipululu mpaka ku Lebanoni, ndi ku Mtsinje wa
Yufurate mpaka ku nyanja ya kumadzulo. 25 Palibe munthu amene
adzalimbana nanu. Monga analonjezera, Yehova adzachititsa kuti anthu
onse m'dziko limene mukupitalo adzachite nanu mantha ndi kukuopani.

26 Taonani, lero ndikuyika dalitso ndi temberero pakati panu, 27 dalitso
ngati mumvera malamulo a Yehova Mulungu wanu amene ndikukupat-
sani lero. 28 Temberero ngati simumvera malamulo a Yehova Mulungu

wanu ndi kupatuka pa njira imene ndikulamulirani lero potsata milungu
ina imene simunayidziwe. 29 Yehova Mulungu wanu akakakufikitsani
m'dziko mukukalandalo kuti mulowemo mukanene za madalitso pa Phiri
la Gerizimu, ndi za matemberero pa Phiri la Ebala. 30 Monga mudziwa,
mapiriwa ali kutsidya kwa Yorodani, kumadzulo kolowera dzuwa, kufupi
ndi mitengo ya thundu ya More, m'dziko la Akanaani aja okhala ku
Araba moyang'anana ndi Giligala. 31 Mwatsala pang'ono kuwoloka
Yorodani kuti mulowe ndi kutenga dziko limene Yehova Mulungu wanu
akukupatsani. Mukadzalitenga dzikolo ndi kukhalamo, 32 mudzaonetsetse
kuti mukumvera malangizo ndi malamulo amene ndikukuwuzani lero.

# 12

*Malo Amodzi Opembedzera*

1 Awa ndi malangizo ndi malamulo amene muyenera kusamalitsanso
kuti muwatsatire m'dziko limene Yehova Mulungu wa makolo anu
wakupatsani kuti mutenge pa nthawi yonse imene muti mudzakhale
m'dzikomo. 2 Muwonongeretu kwathunthu malo onse a pamwamba pa
mapiri ataliatali ndi pa mapiri ang'onoang'ono ndi pansi pa mtengo uli-
wonse wotambalala pamene mitundu imene muyilande dzikolo ankapem-
bedzerapo milungu yawo. 3 Mugumule maguwa awo ansembe, ndi
kuphwanya miyala yawo yachipembedzo ndipo mutenthe pa moto mafano
awo a Asera: mugwetse mafano a milungu yawo ndi kufafaniza mayina
awo m'malo amenewo.

4 Musapembedze Yehova Mulungu wanu monga mmene amachitira
iwowa. 5 Koma inu muzifunafuna kumalo kumene Yehova Mulungu wanu
adzasankhe pakati pa mafuko anu kuti ayikeko dzina lake ndi kukhalako.
Ku malo amenewa muyenera kupitako. 6 Kumeneko muzipititsako
zopereka zanu ndi nsembe zanu zopsereza, ndi chakhumi chanu ndi
mphatso zapadera zimene munalonjeza kupereka ndi zopereka zanu
zaufulu ndi ana oyamba a ng'ombe zanu ndi nkhosa zanu. 7 Kumeneko,
pamaso pa Yehova Mulungu wanu, inu ndi mabanja anu mudzadya ndi
kusangalalako pa china chilichonse chimene mudzakhudza, chifukwa
Yehova Mulungu wanu wakudalitsani.

8 Musadzachite monga tikuchitira lero lino, aliyense kumachita zimene
akuona kuti ndi zoyenera, 9 pakuti simunafike ku malo opumulirako ndi ku
cholowa chimene Yehova Mulungu wanu akukupatsani. 10 Koma mudza-
woloka Yorodani ndi kukhazikika m'dziko limene Yehova Mulungu wanu
akukupatsani ngati cholowa chanu, ndipo Iye adzakupatsani inu mpumulo
ku adani anu okuzungulirani kuti mukhale motchinjirizidwa. 11 Tsono
kumalo kumene Yehova Mulungu wanu adzasankhe kuti azikhalako
muzikabweretsako chilichonse chimene ndikulamulirani inu: zopereka
ndi nsembe zanu zopsereza, chakhumi chanu ndi mphatso zapadera, ndi
chuma chanu chonse chosankhika chimene munalonjeza kwa Yehova.
12 Ndipo kumeneko inu mukasangalale pamaso pa Yehova Mulungu
wanu pamodzi ndi ana anu aamuna ndi ana anu aakazi, antchito anu
aamuna ndi adzakazi anu, ndi Alevi a m'midzi yanu, amene alibe gawo
kapena cholowa chawochawo. 13 Musamalitse kuti musakaphere nsembe
zanu zopsereza paliponse pamene mungafune. 14 Mukaphere pa malo
okhawo amene Yehova adzawasankhe mwa limodzi la mafuko anu, ndipo
kumeneko mukasunge chilichonse chimene ndikulamulireni.

[15] Koma mukhoza kumapha ziweto zanu m'mizinda iliyonse ndi kudya
nyama yake mmene mungafunire, ngati kuti ndi agwape kapena mbawala,
monga mwadalitso limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani. Woy-
eretsedwa ndi wosayeretsedwa akhoza kuyidya. [16] Koma musamadye
magazi. Muziwathira pansi ngati madzi. [17] Musamadyere m'mizinda
yanu chakhumi cha tirigu wanu ndi vinyo watsopano ndi mafuta, kapena
za ana oyamba kubadwa a ng'ombe zanu ndi nkhosa zanu, kapena
chilichonse chimene mwalonjeza kuchipereka, nsembe zanu zaufulu,
kapena mphatso zapadera, [18] m'malo mwake, muzidya pamaso pa Yehova
Mulungu wanu, kumalo kumene Yehova Mulungu wanu adzasankhira inu,
ana anu aamuna ndi aakazi, antchito anu aamuna ndi adzakazi anu, ndi
Alevi ochokera m'mizinda yanu, ndipo mudzasangalale pamaso pa Yehova
Mulungu wanu pa chilichonse chimene mudzachikhudza. [19] Muonetsetse
kuti musawataye Alevi pa masiku onse amene mukhale m'dziko lanumo.

[20] Yehova Mulungu wanu akadzakulitsa dziko lanu monga anaku-
lonjezerani, ndipo mukapukwa nyama mumanena kuti, "Ndikufuna
nyama," pamenepo mudzadya mmene mungafunire. [21] Ngati malo
amene Yehova Mulungu wanu awasankha kuti ayike Dzina lake ali
kutali kwambiri ndi inu, mukhoza kupha ziweto pakati pa ng'ombe
ndi nkhosa zimene Yehova wakupatsani, monga ndinakulamulani, ndipo
m'mizinda yanuyanu mukhoza kuzidya mmene mungafunire. [22] Muzidye
ngati mukudya gwape kapena mbawala. Onse oyeretsedwa monga mwa
mwambo ndi osayeretsedwa omwe akhoza kudya. [23] Koma muonetsetse
kuti musadye magazi, chifukwa magazi ndi moyo, ndipo musamadye
moyo pamodzi ndi nyama. [24] Inu musamadye magazi, muziwathira pansi
ngati madzi. [25] Musamadye magazi kuti zikuyendereni bwino inu pamodzi
ndi ana anu a pambuyo panu, popeza mudzakhala mukuchita zoyenera
pamaso pa Mulungu.

[26] Koma mutenge zinthu zanu zoyeretsedwa ndi china chilichonse
chimene munalumbira kupereka, ndi kupita kumalo kumene Yehova
adzasankhe. [27] Mupereke nsembe zanu zopsereza pa guwa lansembe la
Yehova Mulungu wanu, nyama pamodzi ndi magazi omwe. Magazi a
nsembe zanu athiridwe pambali pa guwa lansembe la Yehova Mulungu
wanu, koma nyamayo mukhoza kudya. [28] Onetsetsani kuti muzimvera
mawu onsewa amene ndikukupatsani kuti zinthu zizikuyenderani bwino
nthawi zonse inu ndi ana anu chifukwa mudzakhala mukuchita zabwino
ndi zoyenera pamaso pa Yehova Mulungu wanu.

[29] Yehova Mulungu wanu adzachotsa pamaso panu mitundu ya anthu
amene mukufuna kuwathira nkhondo ndi kuwalanda dzikolo. Koma
mukawapirikitsa ndi kukhazikika m'dziko lawo, [30] ndipo pamene iwo
awonongeka pamaso panu, samalirani kuti musakodwe mu msam-
pha pa kufufuza za milungu yawo, n'kumati, "Kodi anthu a mitun-
duwa amatumikira bwanji milungu yawo? Ifenso tichita momwemo."
[31] Musapembedze Yehova Mulungu wanu momwe amachitira iwowo,
chifukwa popembedza milungu yawoyo amachita zonyansa zamitundu-
mitundu zimene Yehova amadana nazo. Amatentha ngakhale ana awo
aamuna ndi aakazi pa moto ngati nsembe za kwa milungu yawo.

[32] Onetsetsani kuti mukuchita zimene ndikukulamulirani. Musawonjez-
erepo kapena kuchotserapo.

# 13

*Kupembedza Milungu Ina*

1 Ngati mneneri kapena wina aliyense amene amanena zam'tsogolo
mwa maloto atuluka pakati panu, nalengeza za chizindikiro chozizwitsa
kapena chodabwitsa, 2 chinthu n'kuchitikadi, tsono iyeyo n'kunena kuti,
"Tiyeni titsatire milungu ina, tiyeni tiyipembedze," (kunena milungu
imene simunayidziwe), 3 musamumvere mneneriyo kapena wolotayo.
Yehova Mulungu wanu afuna akuyeseni kuti aone ngati mumamukonda
ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse. 4 Muyenera kutsatira
Yehova Mulungu wanu, ndipo ndi Iyeyo amene muyenera kumuopa.
Muzisunga malamulo ake ndi kumamumvera, muzimutumikira ndipo
kumukangamira Iyeyo. 5 Mneneri kapena wolotayo ayenera kuphedwa,
popeza analalikira zopandukira Yehova Mulungu wanu, amene anakutu-
lutsani ku Igupto ndi kukupulumutsani ku dziko la ukapolo. Wolalikirayo
anafuna kukupatutsani pa njira imene Yehova Mulungu wanu anakula-
mulirani kuti muyitsatire. Muzichotsa choyipa pakati panu.

6 Ngati m'bale wanu weniweni kapena mwana wanu wamwamuna
kapena wamkazi, kapena mkazi wanu wokondedwa, kapena mn-
zanu wapamtima akukakamizani mwachinsinsi, n'kumati, "Tiyeni tipite
tikapembedze milungu ina" (milungu imene inuyo kapena makolo anu
sanayidziwe, 7 milungu ya anthu okuzungulirani, kaya ndi apafupi
kapena akutali, kuchokera kumapeto mpaka kumapeto kwina kwa dziko
lapansi), 8 musamugonjere kapena kumumvera. Musamumvere chisoni.
Musamuleke kapena kumutchinjiriza. 9 Mumuphe ndithu. Dzanja
lanu likhale loyambirira kumupha, kenaka manja a anthu ena onse.
10 Mumuponye miyala mpaka kumupha, chifukwa anafuna kukupatutsani
pa njira ya Yehova Mulungu amene anakutulutsani ku Igupto, dziko la
ukapolo. 11 Tsono Aisraeli onse adzamva nachita mantha, ndipo palibe
mmodzi pakati panu amene adzachitenso choyipa chotere.

12 Ngati mumvetsedwa kuti ku umodzi mwa mizinda imene Yehova Mu-
lungu wanu akukupatsani kuti mukhalemo, 13 kwapezeka anthu ena oyipa
pakati panu ndipo asocheretsa anthu ambiri m'mizinda yanu, pomanena
kuti, "Tiyeni tikapembedze milungu ina" (milungu imene simunayidziwe),
14 mukuyenera kufunsa, kulondola ndi kufufuza bwino nkhaniyo. Ndipo
ngati zitatsimikizikadi kuti ndi zoona kuti chinthu chonyansa chotere
chachitikadi pakati panu, 15 muyenera kuwapha onse okhala mu mzinda
umenewo. Muwonongeretu kwathunthu mzindawo, anthu ake ndi ziweto
zake zomwe. 16 Katundu yense wa anthu mu mzindawo mumuwunjike
pamodzi pakatikati pa bwalo losonkhanako ndipo mutenthe mzindawo
pamodzi ndi katundu wake yense monga nsembe yathunthu yopsereza
ya kwa Yehova Mulungu wanu. Mzinda umenewo ukhale bwinja mpaka
muyaya, usadzamangidwenso. 17 Musapezeke ndi kanthu kalikonse
koyenera kuwonongedwa kuti Yehova abweze mkwiyo wake wochititsa
manthawu. Adzakuchitirani chifundo ndi kukumverani chisoni, ndipo
adzakuchulukitsani monga analonjeza mwa lumbiro kwa makolo anu,
18 chifukwa mumamvera Yehova Mulungu wanu, kusunga malamulo ake
onse amene ndikukupatsani lero lino ndi kuchita zoyenera pamaso pake.

# 14

*Zoletsedwa pa Maliro*

1 Inu ndinu ana a Yehova Mulungu wanu. Osamadzichekacheka kapena
kudzimeta pamphumi chifukwa cha abale anu amene amwalira, 2 pakuti
ndinu anthu opatulika a Yehova Mulungu wanu. Pakati pa anthu onse
pa dziko lonse lapansi, Yehova wasankha inu kuti chikhale chuma chake
chamtengo wapatali.

3 Musamadye chinthu chilichonse chonyansa. 4 Nyama zomwe mukhoza
kudya ndi izi: ng'ombe, nkhosa, mbuzi, 5 mbawala, gwape, mphoyo,
mphalapala, ngoma, nyumbu ndi mbalale. 6 Nyama iliyonse imene
ili ndi chipondero chogawikana pakati ndi yobzikula mukhoza kudya.
7 Komabe pakati pa nyama zimene zimabzikula kapena zogawikana
zipondero, zimene simukuyenera kudya ndi ngamira, kalulu ndi mbira.
Zimenezi ngakhale zimabzikula, zipondero zake sizogawikana, choncho
ndi zodetsedwa, musadye. 8 Nkhumba simabzikula ndi yodetsedwanso
ngakhale ili ndi zipondero zogawikana. Musamadye nyama yake kapena
kukhudza imene yafa.

9 Mwa zamoyo zonse zimene zimakhala m'madzi, mukhoza kudya
chilichonse chimene chili ndi minga ya pa msana ndi mamba. 10 Koma
chilichonse chimene chilibe minga ya pa msana ndi mamba musadye
pakuti n'chodetsedwa.

11 Mukhoza kudya mbalame iliyonse yoyenera kudya. 12 Koma
simukuyenera kudya izi: mphungu, nkhwazi, mwimba, 13 nankapakapa,
akamtema, akhungubwi a mitundu yonse, ndi mtundu uliwonse wa
miphamba, 14 mtundu uliwonse wa khwangwala, 15 kadzidzi wamphondo,
kadzidzi wodzuma, chipudo, mtundu uliwonse wa akabawi, 16 kadzidzi
wamng'ono, chiswankhono ndi mantchichi, 17 tsekwe, vuwo, dembo,
18 indwa, zimeza za mitundu yonse, nsadzu ndi mleme.

19 Zowuluka zonse za miyendo inayi ndi zodetsedwa. Musamadye
zimenezi. 20 Koma chowuluka chilichonse choyenera kudya mukhoza
kudya.

21 Musamadye chilichonse chimene mwachipeza chofaifa. Mukhoza
kupatsa mlendo amene akukhala mu mzinda wina uliwonse wa mizinda
yanu. Iyeyo akhoza kudya kapena mukhoza kugulitsa kwa wina aliyense
amene sali wa mtundu wanu. Koma inu ndinu anthu opatulika a Yehova
Mulungu wanu.

Musamaphike mwana wambuzi mu mkaka wa mayi wake.

### *Za Chakhumi*

22 Muzionetsetsa kuti mukupatula chakhumi pa zokolola zanu chaka
chilichonse. 23 Muzidyera chakhumi cha tirigu wanu, vinyo wanu
watsopano ndi mafuta, ndi ana oyamba kubadwa a ng'ombe zanu pamaso
pa Yehova Mulungu wanu pa malo amene adzasankhe ngati kokhalako
dzina lake, kuti muphunzire kuopa Yehova Mulungu wanu. 24 Koma
ngati malo amenewa ali kutali kwambiri ndipo kuti inu mwadalitsidwa
ndi Yehova Mulungu wanu, ndipo simungathe kunyamula chakhumi
chanu (chifukwa chakuti malo amene Yehova adzasankha kukayikako
dzina lake ali kutali kwambiri), 25 ndiye musinthitse chakhumi chanucho
ndi siliva, ndipo mutenge silivayo ndi kupita naye kumalo kumene
Yehova Mulungu wanu adzasankhe. 26 Gwiritsani ntchito silivayo kugula
chilichonse chimene muchifuna monga ng'ombe, nkhosa, vinyo kapena
zakumwa zina zosasitsa, kapena china chilichonse chimene muchifuna.
Ndipo inu ndi anthu a pa banja panu mudzazidyera komweko pamaso

pa Yehova Mulungu wanu ndi kukondwera. 27 Alevi okhala m'mizinda
yanu musaleke kuwathandiza popeza alibe gawo lawo la chuma kapena
cholowa chawochawo.
28 Kumapeto kwa zaka zitatu zilizonse muzibweretsa zakhumi zonse
pa zokolola za chaka chimenecho ndi kuzisunga m'midzi yanu, 29 kuti
Alevi (amene alibe gawo lawo la chuma kapena cholowa chawochawo),
alendo, ana ndi akazi amasiye, amene akukhala m'mizinda yanu akhoza
kubwera kudzadya ndi kukhuta. Ndipo kuti akutero Yehova Mulungu
wanu akudalitseni pa ntchito zanu zonse.

# 15

### *Chaka Chokhululukira Ngongole*

1 Kumapeto kwa zaka zisanu ndi ziwiri zilizonse, muzikhululuki-
rana ngongole. 2 Zimenezi muzichita motere: wobwereketsa aliyense
adzakhululukira ngongole imene anabwereketsa kwa Mwisraeli mn-
zake. Iye asadzafunenso kuti Mwisraeli mnzakeyo kapena m'bale wake
amubwezere chifukwa nthawi ya Ambuye yokhululukirana ngongole
yalengezedwa. 3 Mukhoza kulonjerera ngongole kwa mlendo, koma
mukhululukire ngongole ina iliyonse imene m'bale wanu ali nayo.
4 Komabe pasadzakhale wosauka pakati panu chifukwa Yehova Mulungu
wanu adzakudalitsani kwambiri m'dziko limene adzakupatsani kuti
likhale lanu ngati cholowa chanu. 5 Adzakudalitsani pokhapokha ngati
mudzamveradi Yehova Mulungu wanu posunga ndi kutsatira malamulo
onse amene ndikukupatsani lero. 6 Pakuti Yehova Mulungu wanu
adzakudalitsani monga analonjeza, ndipo inu mudzabwereketsa chuma
kwa mitundu yambiri ya anthu koma inu simudzabwereka kwa aliyense.
Mudzalamulira mitundu yambiri ya anthu koma inuyo palibe amene
adzakulamulireni.
7 Ngati pali m'bale wanu wina wosauka mu mzinda wanu wina uliwonse
m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani, musawumitse
mitima yanu kapena kuchita kaligwiritsa kwa m'bale wanu wosaukayo.
8 Koma mukhale ofewa manja ndipo mumukongoze m'bale wanu moma-
suka pa chilichonse chimene akufuna. 9 Musayesere ndi pang'ono pomwe
kusunga maganizo oyipa awa mu mtima mwanu: "Chaka chachisanu
ndi chiwiri, chaka chokhululukirana ngongole, chayandikira," kuti
musaonetse mtima woyipa kwa m'bale wanu wosauka n'kusamupatsa
chilichonse. Iye angadzakunenereni inu mlandu kwa Ambuye, ndipo
mudzapezeka wochimwa. 10 Mumupatse iye mowolowamanja ndipo
muchite zimenezi mosasungira kanthu kumtima. Tsono chifukwa cha
zimenezi, Yehova Mulungu wanu adzakudalitsani pa ntchito zanu zonse
ndi pa chilichonse chimene mukhudza. 11 Anthu osauka sadzatha m'dziko
lanu. Chomwecho ndikukulamulani kuti mukhale ofewa manja kwa abale
anu ndi kwa osauka, osowa m'dziko mwanu.

### *Kumasula Akapolo a Chihebri*

12 Ngati m'bale wanu wamwamuna kapena wamkazi adzigulitsa yekha
kwa inu, nakugwirirani ntchito zaka zisanu ndi chimodzi, muzimumasula
m'chaka cha chisanu ndi chiwiri. 13 Ndipo pamene mumumasula,
musangomulola apite chimanjamanja. 14 Mumupatse mowolowamanja
zochokera pa ziweto zanu, kopunthira tirigu ndi kopsinyira vinyo.
Inu mumupatse iye monga Yehova Mulungu wanu wakudalitsirani.
15 Kumbukirani kuti munali akapolo m'dziko la Igupto ndipo Yehova

Mulungu wanu anakupulumutsani. N'chifukwa chake ndikukupatsani
lamulo ili lero lino.
16 Koma ngati kapoloyo akuwuzani kuti, "Ine sindikufuna kuma-
sulidwa," chifukwa choti wakukondani inuyo pamodzi ndi banja lanu
ndiponso kuti kwamukomera iyeyo kuti azikhalabe nanu, 17 pamenepo
muzitenga chobowolera chachitsulo ndi kubowola khutu lake pa chitseko,
ndipo mukatero adzakhala kapolo wanu moyo wake wonse. Mdzakazi
wanu muzimuchitanso chimodzimodzi.
18 Musaone ngati chopweteka kumasula wantchito wanu, chifukwa
ntchito imene wayigwira pa zaka zisanu ndi chimodzi zimenezi ndi yopin-
dula kawiri pa ntchito imene akanagwira waganyu chabe. Ndipo Yehova
Mulungu wanu adzakudalitsani pa chilichonse chimene mukuchita.

### *Ziweto Zoyamba Kubadwa*

19 Mumupatulire Yehova Mulungu wanu choyamba kubadwa
chachimuna chilichonse pa ng'ombe ndi nkhosa zanu. Musamazigwiritse
ntchito ng'ombe zoyamba kubadwa kapena kumeta nkhosa zoyamba
kubadwa. 20 Inuyo ndi banja lanu, chaka chilichonse muzizidya zimenezi
pamaso pa Yehova Mulungu wanu pa malo amene Iye adzasankhe.
21 Ngati chiweto chili ndi chilema monga kulumala kapena chosaona,
kapena ngati chili ndi cholakwika chachikulu chilichonse, musachipereke
nsembe kwa Yehova Mulungu wanu. 22 Muzichidya m'mizinda yanuyanu.
Onse odetsedwa monga mwa mwambo ndi oyeretsedwa omwe akhoza
kuchidya monga akudya gwape kapena mbawala. 23 Koma musadye
magazi ake. Muwathire pansi ngati madzi.

## 16

### *Paska*

1 Samalirani mwezi wa Abibu ndi kukondwerera Paska wa Yehova
Mulungu wanu, chifukwa pa mwezi wa Abibu, usiku, Iye anakutulutsani
mu Igupto. 2 Mumuphere Yehova Mulungu wanu nsembe ya Paska,
chiweto chochokera pa nkhosa zanu kapena ng'ombe zanu kumalo
kumene Yehova adzasankha kuti akhazikeko dzina lake. 3 Musadyere
pamodzi ndi buledi wopanga ndi yisiti, koma kwa masiku asanu ndi
awiri muzidya buledi wopanda yisiti, buledi wa masautso, chifukwa
munachoka ku Igupto mwamsangamsanga kuti pa masiku onse a moyo
wanu muzikumbukira nthawi imene munanyamukira ku Igupto. 4 Yisiti
asapezeke kwa masiku asanu ndi awiri pa katundu wanu m'dziko lanu
lonse. Ndipo musasunge nyama imene mwapereka nsembe madzulo a
tsiku loyamba mpaka mmawa.
5 Musamangopereka nsembe ya Paska mu mzinda wina uliwonse
umene Yehova Mulungu wanu wakupatsani, 6 koma ku malo wokhawo
amene Iye adzawasankhe kukhazikitsako Dzina lake. Kumeneko ndiye
muzikapereka nsembe ya Paska madzulo, pamene dzuwa likulowa, pa
tsiku lokumbukira kutuluka mu Igupto. 7 Muyiwotche ndi kuyidya pa malo
pamene Yehova Mulungu wanu adzasankhe. Kenaka mmawa mubwerere
ku matenti anu. 8 Kwa masiku asanu ndi limodzi muzidya buledi wopanda
yisiti ndipo pa tsiku lachisanu ndi chiwiri muzikhala ndi msonkhano wa
Yehova Mulungu wanu ndipo musamagwire ntchito iliyonse.

### *Chikondwerero cha Masabata*

9 Muziwerenga masabata asanu ndi awiri kuyambira pamene mwa-
tenga chikwakwa ndi kuyamba kumweta tirigu wachilili. 10 Pamenepo
muzichita Chikondwerero cha Masabata pamaso pa Yehova Mulungu
wanu popereka chopereka chaufulu mofanana ndi madalitso amene
Yehova Mulungu wakupatsani 11 Ndipo inu, ana anu aamuna, aakazi,
antchito anu aamuna, adzakazi, Alevi a m'mizinda mwanu, alendo, ana
ndi akazi amasiye okhala pakati panu, mukondwere pamaso pa Yehova
Mulungu wanu ku malo amene adzawasankhe kukhazikitsako dzina lake.
12 Kumbukirani kuti inunso munali akapolo ku Igupto, ndiye muzitsatira
malangizo awa mosamalitsa.

### *Chikondwerero cha Misasa*

13 Mukatha kukolola tirigu wanu ndi kupsinya vinyo wanu,
muzikhala ndi Chikondwerero cha Misasa kwa masiku asanu ndi awiri.
14 Musangalale pa chikondwerero chanu, inu, ana anu aamuna, aakazi,
antchito anu aamuna, adzakazi, Alevi, alendo, ana ndi akazi amasiye
amene ali m'mizinda yanu. 15 Kwa masiku asanu ndi awiri muzichita
chikondwererochi kwa Yehova Mulungu wanu kumalo kumene Yehova
adzasankhe. Pakuti Yehova Mulungu wanu adzakudalitsani inu pa
zokolola zanu ndi pa ntchito za manja anu, ndipo chimwemwe chanu
chidzakhala chathunthu.
16 Amuna onse azionekera pamaso pa Yehova Mulungu katatu pa chaka
ku malo amene Iye adzasankha. Pa Chikondwerero cha Buledi wopanda
Yisiti, pa Chikondwerero cha Masabata ndi pa Chikondwerero cha Misasa.
Munthu aliyense asadzapite pamaso pa Yehova wopanda kanthu m'manja
mwake. 17 Aliyense wa inu adzabweretse mphatso molingana ndi momwe
Yehova Mulungu wanu wakudalitsirani.

### *Oweruza*

18 Musankhe oweruza ndi akuluakulu a fuko lanu lililonse mu mzinda
uliwonse umene Yehova Mulungu wanu akukupatsani, ndipo adzaweruza
anthuwa mwachilungamo. 19 Musamakhotetse chiweruzo kapena kukon-
dera. Musamalandire chiphuphu pakuti chiphuphu chimadetsa m'maso
anthu a nzeru ndi kusintha mawu awo kuti mlandu uyipire osalakwa.
20 Tsatani chilungamo chokhachokha basi kuti mukhale ndi moyo ndi
kutenga dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani.

### *Kupembedza Milungu Ina*

21 Musazike mtengo wina uliwonse wa mafano a Asera pambali pa
guwa lansembe la Yehova Mulungu wanu, 22 ndipo musayimike mwala
wachipembedzo pakuti Yehova Mulungu wanu amadana nazo zimenezi.

## 17

1 Musapereke nsembe kwa Yehova Mulungu wanu ng'ombe kapena
nkhosa imene ili ndi chilema kapena cholakwika chilichonse, pakuti
zimenezi zimamunyansa.
2 Ngati mwamuna kapena mkazi pakati panu, m'mizinda imene Yehova
akukupatsani apezeka akuchita zoyipa pamaso pa Yehova Mulungu wanu
pophwanya pangano lake, 3 ndipo ngati motsutsana ndi lamulo langa
wapembedza milungu ina, kuyigwadira milunguyo, kaya ndi dzuwa
kapena mwezi kapena nyenyezi zakumwamba, 4 ndipo inu n'kuwuzidwa
zimenezi, mufufuze bwinobwino. Ngati ndi zoona, ndipo ngati zatsimik-
izika kuti chonyansa choterechi chachitikadi mu Israeli, 5 mumutengere
mwamuna kapena mkazi amene wachita chonyansa choterechi ku chipata

cha mzinda wanu ndi kumupha pomugenda miyala. 6 Munthu aziphedwa
pakakhala mboni ziwiri kapena zitatu koma osati mboni imodzi yokha
ayi. 7 Wochitira umboniwo ndiwo aziyamba kumupha munthuyo, ndipo
kenaka anthu onse. Muyenera kuchotsa choyipa pakati panu.

*Mabwalo a Milandu*

8 Ngati akubweretserani milandu m'mabwalo anu imene ili yovuta
kuweruza kaya ndi yokhetsa magazi, kaya ndi yophwanyirana ufulu, kaya
ndi yovulazana, muyitengere kumalo kumene Yehova Mulungu wanu
adzasankhe. 9 Mudzapite kwa ansembe Alevi ndi kwa woweruza wa
pa nthawi imeneyo. Kawafunseni ndipo iwowo adzakuwuzani zoyenera
kuchita. 10 Kachiteni zimene adzakuwuzenizo kuchokera ku malo
amene Yehova adzasankhe. Kaonetsetseni kuti mukutsatira zonse zimene
akuwuzanizo. 11 Kachiteni motsatira malamulo ndi malangizo amene
adzakuwuzeni; osawanyoza, potembenukira kumanja kapena kumanzere.
12 Munthu aliyense amene adzanyoza woweruza kapena wansembe
amene akutumikira kumeneko m'malo mwa Yehova Mulungu wanu,
aphedwe ndithu. Muzichotsa choyipa pakati pa Israeli. 13 Anthu onse
adzamva zimenezi ndipo adzachita mantha, choncho sadzadzikuzanso.

*Mfumu*

14 Mukalowa m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani
kuti mulitenge, ndipo mukakakhazikika m'menemo nimunena kuti,
"Tiyeni tisankhe mfumu yoti izitilamulira monga imachitira mitundu
yonse yotizungulirayi," 15 mudzakhazikitse mfumu yoti izikakulamulirani,
mfumu imene Yehova Mulungu wanu adzasankhe pakati panu. Mudza-
sankhe mfumuyo kuchokera pakati pa abale anu. Osasankha mlendo,
munthu amene sachokera pakati pa abale anu Aisraeli. 16 Komatu
mfumuyo isadzikundikire akavalo, kapena kutuma anthu kupita ku
Igupto kukayipezera akavalo ena, pakuti Ambuye akuti, "Simuyenera
kubweranso ku Igupto m'njira yomweyo." 17 Asadziwunjikire akazi kuopa
kuti mtima wake ungamusocheretse. Asadziwunjikirenso golide ndi siliva
wambiri.
18 Akakhala pa mpando waufumuwo, ayenera kulemba za iye mwini
m'buku la malamuloli, kuchokera kwa ansembe Alevi. 19 Asunge zimene
walembazo ndipo ayenera kumaziwerenga masiku onse a moyo wake, kuti
aphunzire kuopa Yehova Mulungu wake posunga mosamalitsa malamulo
ndi malangizowa. 20 Asadzione kuti iyeyo ndi wopambana kuposa abale
ake, nalekeratu kutsatira malamulo. Akasamala zimenezi iye ndi ana ake
adzalamulira ufumu wa Israeli kwa nthawi yayitali.

# 18

*Zopereka za kwa Ansembe ndi Alevi*

1 Ansembe Achilevi amene ndi fuko lonse la Alevi, asapatsidwe malo
kapena cholowa pakati pa Aisraeli. Iwowa azidzadya zoperekedwa kwa
Yehova ngati nsembe, popeza zimenezo ndiye cholowa chawo. 2 Iwowa
sadzakhala ndi cholowa pakati pa abale awo pakuti Yehova ndiye cholowa
chawo monga anawalonjezera.
3 Anthu amene abwera kudzapereka nsembe ya ng'ombe kapena
nkhosa, azipereka kwa wansembe gawo lake motere: mwendo wakutso-
golo, nyama yam'masaya ndi zam'kati. 4 Muziwapatsa zamasika zoyamba
za tirigu wanu, vinyo watsopano ndi mafuta, ndi ubweya woyamba

pometa nkhosa zanu, [5] pakuti Yehova Mulungu wanu wawasankha iwowa
ndi ana awo pakati pa mafuko anu onse kuti aziyimirira ndi kutumikira
m'dzina la Yehova nthawi zonse.
[6] Ngati Mlevi asuntha achoka ku mzinda wake ndi kupita kumalo kwina
kumene Yehova wasankha mu Israeli momwemo ndi mtima wake wonse,
[7] kumeneko akhoza kukatumikirako m'dzina la Yehova Mulungu wake
monga Alevi anzake onse amene akutumikira pamaso pa Yehova. [8] Iye
ayenera kulandira zogawana zawo mofanana ndi anzakewo ngakhale kuti
iye anagulitsa kale cholowa cha pa banja pawo.

*Makhalidwe Oletsedwa*

[9] Mukafika m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani,
musakaphunzire makhalidwe onyansa a anthu a m'dzikolo. [10] Pasapezeke
pakati panu munthu wootcha pa moto mwana wake wamwamuna kapena
wamkazi ngati nsembe. Asapezekenso pakati panu munthu wowombeza
kapena wochita mawula, wolosera, wochita za ufiti, [11] wolodza, kapena
woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa ndi kumafunsira nzeru kwa anthu
akufawo. [12] Aliyense wochita zinthu zotere ndi wonyansa pamaso pa
Yehova, ndipo chifukwa cha zonyansa zimenezi Yehova adzakupirikitsir-
ani mitundu ya anthu imeneyi. [13] Muzikhala angwiro pamaso pa Yehova
Mulungu wanu.

*Aneneri*

[14] Mitundu ya anthu imene mudzayipirikitseyo imamvera anyanga
kapena owombeza mawula. Koma inu Yehova Mulungu wanu sanaku-
vomerezeni kutero. [15] Yehova Mulungu wanu adzawutsa pakati pa abale
anu mneneri ngati ine. Muyenera kumumvera ameneyo. [16] Pakuti izi ndi
zimene munapempha kwa Yehova Mulungu wanu ku Horebu pa tsiku la
msonkhano lija pamene munati, "Ife tisamvenso mawu a Yehova Mulungu
wathu kapena kuona moto woopsawu, kuopa kuti tingafe."
[17] Yehova anati kwa ine, "Zimene akunenazi ndi zabwino.
[18] Ndidzawawutsira mneneri ngati iwe pakati pa abale awo ndipo
ndidzayika mawu anga m'kamwa mwake ndipo adzawawuza chilichonse
chimene ndidzamulamula. [19] Ine mwini ndidzaweruza aliyense amene
sadzamvera mawu anga amene mneneriyo adzayankhula m'dzina langa.
[20] Koma mneneri wonena zinthu m'dzina langa ndisanamulamulire
kutero, kapena mneneri wonenera m'dzina la milungu ina, ayenera
kuphedwa."
[21] Mwina mukhoza kumadzifunsa kuti, "Kodi tingadziwe bwanji kuti
uthengawu sanayankhule ndi Yehova?" [22] Ngati zimene mneneriyo
wanenera m'dzina la Yehova sizinachitike kapena kukwaniritsidwa, ndiye
kuti umenewo si uthenga umene Yehova wayankhula. Mneneri ameneyo
amangoyankhula za m'mutu mwake ndiye musadzidzimuke naye.

## 19

*Mizinda Yothawirako*

[1] Yehova Mulungu wanu akadzawononga anthu amene dziko lawo
akukupatsani, ndipo inu mukawapirikitsa ndi kukhazikika m'mizinda
ndi m'nyumba zawo, [2] mukapatule mizinda itatu imene ili pakati pa
dziko lomwe Yehova Mulungu akukupatsani kukhala lanu. [3] Mudzakonze
misewu ndi kuligawa patatu dzikolo limene Yehova Mulungu wanu

akukupatsani ngati cholowa chanu, kuti aliyense wopha munthu akhoza kuthawirako.

[4] Ili ndi lamulo lokhudza munthu amene wapha mnzake mosazindikira
osati mwadala, nathawira kumeneko kupulumutsa moyo wake. Ndi
munthu amene wapha mnzake mosazindikira, popanda maganizo oyipa.
[5] Mwachitsanzo, munthu atapita ku nkhalango ndi mnzake kukadula
mitengo, ndiye posamula nkhwangwa kuti adule mtengo, nkhwangwa
ikhoza kuguluka n'kukagwera mnzake uja n'kumupha. Munthu ameneyo
akhoza kuthawira ku umodzi mwa mizindayo napulumutsa moyo
wake. [6] Kupanda kutero ndiye kuti wolipsira akhoza kumuthamangitsa
mwaukali ndi kumugwira ngati mtunda utalika, ndipo akhoza kumupha
ngakhale kuti sanayenera kufa popeza sanaphe mnzake mwadala. [7] Ichi
ndi chifukwa chake ndikukulamulani kuti mudzipatulire nokha mizinda
itatu.

[8] Ngati Yehova Mulungu wanu akulitsa malire anu monga analonjezera
pa malumbiro ndi makolo anu, nakupatsani dziko lonse monga analonjez-
era, [9] chifukwa chotsatira bwino malamulo onse amene ndikukuwuzani
lero, kukonda Yehova Mulungu wanu ndi kuyenda m'njira zake nthawi
zonse, ndiye kuti mukuyenera kupatula mizinda itatu yowonjezera.
[10] Muchite zimenezi kuti musakhetse magazi wosalakwa m'dziko lanu
limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani ngati cholowa, ndipo kuti
musapezeke ndi mlandu wokhetsa magazi.

[11] Koma ngati munthu adana ndi mnzake namubisalira panjira
n'kumuvulaza mpaka kumupha, nathawira ku umodzi mwa mizindayi,
[12] akuluakulu a mu mzinda wake akamugwire ndi kumubwezera ku
mzinda wake namupereka kwa wolipsira kuti aphedwe. [13] Osamumvera
chisoni. Muyenera kuchotsa tchimo lokhetsa magazi wosalakwa mu Israeli
kuti zinthu zizikuyenderani bwino.

[14] Musamasunthe mwala wa malire anu ndi mnzanu amene anayikidwa ndi makolo anu pa cholowa chimene mulandire m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani.

### *Mboni*

[15] Mboni imodzi siyokwanira kupeza munthu kuti ndi wolakwa pa mlandu uliwonse umene wapalamula. Nkhani itsimikizike ndi umboni wa anthu awiri kapena atatu.

[16] Ngati mboni yonama ifuna kunamizira munthu mlandu, [17] anthu
awiri okhudzidwa ndi mlanduwo ayenera kuyima pamaso pa Yehova pali
ansembe ndi oweruza amene ali pa ntchito pa nthawiyo. [18] Oweruza
afufuze bwinobwino, ndipo ngati zatsimikizika kuti mboniyo ndi yabodza,
yopereka umboni wonama pa m'bale wake, [19] ndiye kuti amuchitire iyeyo
zimene anafuna kuchitira m'bale wakezo. Muyenera kuchotsa choyipa
pakati panu. [20] Anthu ena onse adzamva zimenezi nachita mantha, ndipo
choyipa choterechi sichidzachitikanso pakati panu. [21] Osachita chisoni,
moyo uzilipira moyo, diso kulipira diso, dzino kulipira dzino, dzanja
kulipira dzanja ndi phazi kulipira phazi.

## 20

### *Za ku Nkhondo*

[1] Pamene mukupita kokachita nkhondo ndi adani anu, mukaona akavalo kapena magaleta kapena gulu la ankhondo kuposa inuyo musamaope

chifukwa Yehova Mulungu wanu, amene anakutulutsani ku Igupto adza-
khala nanu. 2 Pamene mwatsala pang'ono kuyamba nkhondo, wansembe
azibwera kutsogolo ndipo aziyankhula ku gulu lonse lankhondolo. 3 Iye
aziti, "Tamverani inu Aisraeli, mukupita kukachita nkhondo ndi adani anu
lero. Musataye mitima kapena kuchita mantha ayi. Musaopsedwe kapena
kunjenjemera pamaso pawo, 4 pakuti Yehova Mulungu wanu ndiye amene
apite nanu kukakumenyerani nkhondo ndi kugonjetsa adani anu."

5 Akuluakulu ankhondo adzati kwa gulu la ankhondolo, "Kodi pali wina
amene wangomanga nyumba kumene ndipo sanayitsekulire? Ayambe
wapita ku mudzi chifukwa mwina akafera ku nkhondoko ndipo wina
ndi kudzayitsekulira. 6 Kodi pali wina amene analima munda wamphesa
ndipo sanayambe kudyerera? Ayambe wapita ku mudzi chifukwa mwina
akafera ku nkhondo ndipo wina adzadyerera mundawo. 7 Kodi pali amene
wachita chinkhoswe ndi mkazi ndipo sanamukwatire mkaziyo? Ayambe
wabwerera ku mudzi chifukwa mwina akafera ku nkhondo ndipo wina
adzakwatira mkaziyo." 8 Ndipo akuluakulu ankhondowo akapitirize kuti,
"Kodi pali amene akuchita mantha kapena kutaya mtima? Abwerere
ku mudzi kuopa kuti abale ake angatayenso mtima." 9 Akuluakuluwo
akatsiriza kuyankhula ndi gulu la ankhondolo, adzasankhe olilamulira.

10 Pamene mukuyandikira kuphwanya mzinda, muyambe mwafunsa
anthu a mu mzindawo ngati afuna zamtendere. 11 Akavomera natsekula
zipata zawo, anthu wonse mu mzindawo adzagwidwa ukapolo nakug-
wiriran ntchito. 12 Koma akakana za mtendere nachita nanu nkhondo,
muwuphwanye mzindawo. 13 Yehova Mulungu wanu akakupatsani
mzindawo, muwaphe amuna onse. 14 Akazi, ana, ziweto ndi china
chilichonse mu mzindamo, mukhoza kuzitenga kuti zikhale zanu monga
katundu wolanda ku nkhondo. Katundu wa adani anuyu amene Yehova
Mulungu wanu akukupatsani, mukhoza kumugwiritsa ntchito. 15 Mizinda
yonse yakutali osati ya mitundu yapafupi, muzichita nayo chomwechi.

16 Komabe m'mizinda imene Yehova Mulungu wanu akukupatsani ngati
cholowa chanu, musasiyemo chamoyo chilichonse. 17 Muwawononge
kwathunthu Ahiti, Aamori, Akanaani, Aperezi, Ahivi ndi Ayebusi monga
momwe Yehova Mulungu wanu anakulamulirani. 18 Mukapanda kutero
adzakuphunzitsani kuti mutengere zinthu zonyansa zimene amachita
popembedza milungu yawo ndipo mudzachimwira Yehova Mulungu
wanu.

19 Mukalimbana ndi mzinda nthawi yayitali, kuchita nawo nkhondo po-
funa kuwugonjetsa, musawononge podula mitengo yake ndi nkhwangwa,
osayidula chifukwa zipatso zakezo mukhoza kudya. Kodi mitengo ya ku
munda ndi anthu kuti mukalimbane nayo? 20 Komabe mukhoza kudula
mitengo imene mukudziwa kuti si ya zipatso ndi kuyigwiritsa ntchito pa
nkhondo mpaka mzinda umene mukumenyana nawowo utagwetsedwa.

# 21

### *Nsembe Yopepesera Munthu Akaphedwa Mosadziwika Bwino*

1 Ngati munthu apezeka ataphedwa m'munda m'dziko limene Yehova
Mulungu wanu akukupatsani kukhala lanu koma inu osadziwa amene
wamupha, 2 akuluakulu anu ndi oweruza adzapite ndi kuyeza kutalikirana
kuchokera pamene pali mtembowo ndi mizinda yoyandikira. 3 Kenaka
akuluakulu a mzinda wapafupi kwambiri ndi mtembowo adzatenge

ng'ombe imene sinagwirepo ntchito kapena kuvalapo goli [4] ndi kuyikusira
ku chigwa chimene sichinalimidwepo ndiponso kumene kuli mtsinje
woyenda. Ku chigwa kumeneko ayenera kukayithyola khosi ng'ombeyo.
[5] Ansembe, ana a Aaroni, adzapite patsogolo pang'ono, popeza ndiwo
amene Yehova Mulungu wanu anawasankha kuti azitumikira, kupereka
mdalitso m'dzina la Yehova ndi kugamula milandu yonse yamikangano
ndi yovulazana. [6] Kenaka akuluakulu a mzinda wapafupi kwambiri ndi
mtembowo adzasamba m'manja pamwamba pa ng'ombe yothyoledwa
khosi ija, [7] nadzatsimikiza kuti, “Manja athu sanakhetse magazi awa ndipo
sitinaonerere kuphedwako. [8] Yehova, landirani nsembe yopepesa ya anthu
anu Aisraeli amene munawapulumutsa, ndipo muwakhululukire tchimo
la kupha munthu wosalakwa.” Mukatero ndiye kuti adzapezeka kuti
ndi osalakwa. [9] Kotero mudzadzichotsera nokha tchimo lokhetsa magazi
wosalakwa, popeza mwachita zoyenera pamaso pa Yehova.

### *Kukwatira Mkazi Wogwidwa ku Nkhondo*

[10] Mukapita kukachita nkhondo ndi adani anu, Yehova Mulungu wanu
nawapereka adani anuwo m'manja mwanu muwagwira ukapolo, [11] ndiye
ngati muona mkazi wokongola pakati pa ogwidwawo nakutengani mtima,
mukhoza kumutenga kuti akhale mkazi wanu. [12] Mumutengere ku
nyumba kwanu, kumumeta tsitsi lake, mumuwenge zikhadabo zake
[13] ndipo avulidwe zovala zimene anagwidwa nazo. Atakhala m'nyumba
mwanu nalira maliro a abambo ndi amayi ake kwa mwezi wathunthu,
ndiye mukhoza kupita kwa iye ndi kukhala mwamuna wake ndipo iyeyo
adzakhala mkazi wanu. [14] Ngati simukukondweretsedwa naye, muloleni
kuti apite kumene afuna. Musamugulitse kapena kumuzunza ngati
kapolo, popeza mwamuchotsa ulemu.

### *Ufulu wa Mwana Woyamba Kubadwa*

[15] Ngati munthu ali ndi akazi awiri, nakonda wina koposa mnzake,
onsewa ndikubereka ana aamuna koma woyamba nakhala mwana wa
mkazi amene samukondayo, [16] akamagawa chuma chake akanali moyo
kwa ana akewo, asapereke ufulu wa mwana woyamba kubadwa kwa
mwana wamwamuna wa mkazi amene amamukonda m'malo mwa
mwana wake woyamba kubadwa weniweni amene ndi mwana wamkazi
amene samukonda. [17] Iye ayenera kuonetsa kuti mwana wake wamwa-
muna wa mkazi wosakondedwayo ndiye woyamba kubadwa pomupatsa
miyeso iwiri ya zonse zimene ali nazo. Mwana wamwamuna ameneyo
ndiye chizindikiro cha mphamvu za abambo ake. Ufulu wokhala mwana
wamwamuna woyamba ndi wake.

### *Mwana Wamwamuna Wowukira*

[18] Ngati munthu ali ndi mwana wamwamuna wosamvera ndi wowukira
amene samvera a abambo ake ndi amayi ake akamuweruza, [19] abambo
ndi amayi ake amugwire ndi kupita naye kwa akuluakulu ku chipata cha
mzinda wake ndipo [20] akawawuze akuluakuluwo kuti, “Mwana wathu
wamwamunayu ndi wosamva ndi wowukira. Iyeyu satimvera. Ndi
mwana wadyera komanso ndi chidakwa.” [21] Pamenepo anthu onse a mu
mzinda wake adzamuphe ndi miyala. Muyenera kuchotsa zoyipa pakati
panu. Aisraeli onse adzamva zimenezi ndipo adzachita mantha.

### *Malamulo Osiyanasiyana*

22 Ngati munthu wopezeka ndi mlandu wopha mnzake waphedwa ndipo
mtembo wake wapachikidwa pamtengo, 23 musasiye mtembowo pa mten-
gopo usiku wonse. Muonetsetse kuti mwakawukwirira tsiku lomwelo,
chifukwa aliyense wopachikidwa pamtengo ndi wotembereredwa ndi
Mulungu. Musayipitse dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani
ngati cholowa chanu.

# 22

1 Ngati uwona ng’ombe kapena nkhosa ya m’bale wako ikusochera,
usayilekerere koma uyesetse kuyibwezera kwa iye. 2 Ngati m’bale
wakoyo sakhala pafupi kapena sukudziwa kuti ndi yandani, uyitengere
ku nyumba kwako ndi kuyisamala mpaka mwini wake atayilondola ndipo
umubwezere. 3 Uzitero ndithu ngati upeza bulu kapena mkanjo kapena
chilichonse chimene chatayika. Osachilekerera.

4 Ngati wapeza bulu kapena ng’ombe ya m’bale wako itagwa panjira,
usayilekerere. Ithandize kuti idzuke.

5 Akazi asavale zovala za amuna, kapena mwamuna kuvala zovala za akazi, pakuti Yehova Mulungu wanu amanyansidwa ndi aliyense wochita izi.

6 Ukapeza chisa cha mbalame m’mphepete mwa msewu, kaya ndi mu
mtengo kapena pansi, mbalame yayikazi itafungatira ana kapena mazira,
usatenge mbalameyo pamodzi ndi ana ake omwe. 7 Anawo mukhoza
kutenga koma onetsetsani kuti mayi wawo mwamutaya kuti apite, kuti
zinthu zizikuyenderani bwino ndiponso kuti mukhale ndi moyo wautali.

8 Mukamanga nyumba yatsopano, mutchingire khonde lake la pa denga kuti inu musapezeke ndi mlandu wopha munthu ngati wina agwa kuchokera pa khonde la pa dengalo.

9 Musadzale mbewu zamitundu iwiri m’munda wanu wa mpesa, ngati mutero, si mbewu zanu zokha zimene zidzakhale zodetsedwa, komanso zipatso za m’munda wamphesawo.

10 Musatipule pogwiritsa ntchito ng’ombe ndi bulu pa goli limodzi.

11 Musamavale chovala chopangidwa mophatikiza ubweya ndi thonje.

12 Muzipanga mphonje m’ngodya za mkanjo umene mumavala.

*Malamulo a Ukwati*

13 Ngati munthu akwatira mkazi, ndipo atagona naye n’kusamufunanso
14 namunyoza ndi kumuyipitsira dzina n’kumati, “Ine ndinakwatira mkazi
uyu, koma pamene ndinakhala naye, sindinachione chizindikiro cha
unamwali wake,” 15 zikatero abambo ndi amayi ake ayenera kubweretsa
chitsimikizo chakuti anali namwali kwa akuluakulu a mzinda ku chipata.
16 Abambo ake a mtsikanayo adzanene kwa akuluakuluwo kuti, “Ine
ndinamupatsa munthu uyu mwana wanga wamkazi kuti amukwatire,
koma sakumufunanso. 17 Tsopano wamunyoza ndipo wanena kuti, ‘Ine
sindinapeze kuti mwana wanu wamkaziyu ndi namwali.’ Koma tsopano
onani chitsimikizo ichi cha unamwali wa mwana wanga wamkazi.”
Kenaka makolo a mtsikanayo adzaonetse kansalu kwa akuluakulu aja,
18 ndipo akuluakuluwo adzamugwire munthuyo namupatsa chilango.
19 Iwo adzamulipitse ndalama zasiliva zokwana 100 nazipereka kwa
abambo a mtsikana, chifukwa munthu uyu wayipitsa dzina la mtsikana
wa Chiisraeli. Ayenera kukhalabe mkazi wake ndipo asadzamuleke moyo
wake wonse.

[20] Koma ngati zomunenerazo ndi zoona, ndipo kuti chitsimikizo cha
unamwali wa mtsikanayo sichinapezeke, [21] iyeyu ayenera kumutengera
pa khomo pa abambo ake pamene anthu a mu mzinda wake akamuphere
ndi miyala. Iyeyo wachita chinthu chochititsa manyazi mu Israeli pochita
chiwerewere akanali pa khomo pa abambo ake. Muyenera kuchotsa
zoyipa pakati panu.

[22] Ngati munthu apezeka akugona ndi mkazi wa mwini wake, ayenera
kuphedwa munthuyo pamodzi ndi mkazi yemwe wagona nayeyo. Muyen-
era kuchotsa zoyipa mu Israeli.

[23] Ngati munthu mu mzinda akumana ndi mkazi yemwe anachita kale
chinkhoswe nagona naye, [24] muwatengere awiriwo ku chipata cha mzinda
ndi kuwapha ndi miyala. Aphedwe chifukwa mtsikanayo anali pafupi
ndi anthu ndipo sanakuwe kuti ena amuthandize ndipo mwamunayo
chifukwa anayipitsa mkazi wa mwini. Muyenera kuchotsa choyipa pakati
panu.

[25] Koma ngati munthu akumana ndi mkazi kutchire yemwe anachita
kale chinkhoswe namugwiririra, mwamuna yekhayo ndiye woyenera
kuphedwa. [26] Mtsikanayo musamuchite chilichonse, palibe tchimo
limene wachita loti ayenera kuphedwa. Mlandu uwu ufanana ndi wa
munthu amene alimbana ndi kupha mnzake woyandikana naye, [27] pakuti
mwamunayo anamupeza mtsikanayo kutchire, ndipo ngakhale mtsikana
wachinkhosweyo anakuwa, panalibe anamulanditsa.

[28] Ngati munthu apezana ndi namwali woti sanachite chinkhoswe,
namugwiririra, munthuyo n'kupezeka, [29] ayenera kuwalipira abambo ake
a namwaliyo ndalama za siliva makumi asanu. Iye ayenera kumukwatira
mkaziyo chifukwa wamuyipitsa, ndipo sadzamulekanso moyo wake
wonse.

[30] Munthu asakwatire mkazi wa abambo ake pakuti ayenera kuchitira
ulemu pogona pa abambo ake.

# 23

*Wosayenera mu Msonkhano*

[1] Mwamuna aliyense wofulidwa kapena woduka chiwalo chachimuna
asalowe nawo mu msonkhano wa Yehova.

[2] Aliyense wobadwa m'banja losavomerezeka, kapena mdzukulu wake
wina aliyense, ngakhale mibado khumi pambuyo pake, asalowe mu
msonkhano wa Yehova.

[3] Mwamoni kapena Mmowabu asalowe mu msonkhano wa anthu
a Yehova ngakhale mibado khumi yobwera pambuyo pake. [4] Pakuti
iwowa sanabwere kudzakulonjerani ndi chakudya kapena madzi pamene
mumadutsa pochokera ku Igupto, m'malo mwake anakalemba ganyu
Balaamu mwana wa Beori wochokera ku Petori ku Mesopotamiya kuti
akutemberereni. [5] Komabe Yehova Mulungu wanu sanamvere Balaamu
koma anatembenuza temberero kukhala dalitso kwa inu chifukwa Yehova
Mulungu wanu amakukondani. [6] Musachite nawo mgwirizano uliwonse
wa mtendere pa moyo wanu wonse.

[7] Musapeputse Mwedomu pakuti ndi m'bale wanu ndithu. Musapeputse
Mwigupto chifukwa munali alendo m'dziko lake. [8] M'bado wachitatu wa
ana awo akhoza kulowa mu msonkhano wa anthu a Yehova.

*Masamalidwe a Msasa*

9 Mukamakhala pa msasa pokonzekera adani anu, musayandikane
ndi china chilichonse chodetsedwa. 10 Wina mwa asilikali anu akadzi-
wonongera ndi umuna usiku, ayenera kuchoka pa msasapo ndipo akhale
kunja kwa msasa. 11 Koma dzuwa likapendeka ayenera kusamba ndipo
polowa dzuwa akhoza kubwerera ku msasa.

12 Mukonze malo kunja kwa msasa kumene mukhoza
kukadzithandizirako. 13 Pakati pa zida zanu muzikhala ndi china
chokumbira, ndipo pokadzithandiza muzikumba kadzenje ndi kukwirira
chimbudzi chanu. 14 Pakuti Yehova Mulungu wanu amayendayenda
ku msasa wanu kukutchinjirizani ndi kupereka adani anu kwa inu.
N'chifukwa chake msasa wanu uzikhala wopatulika kuti mwina angaone
china chonyansa nabwerera osakuyandikirani.

*Malamulo Osiyanasiyana*

15 Ngati kapolo wathawa mbuye wake nakabisala kwanu, musamu-
perekenso kwa mbuye wakeyo. 16 Mumulole akhale pakati panu,
paliponse pamene angakonde, m'mudzi umene angasankhe ndipo
musamupondereze.

17 Pasapezeke Mwisraeli wamwamuna kapena wamkazi wochita chiw-
erewere ku Nyumba ya Mulungu. 18 Musabweretse malipiro a wachiw-
erewere wamkazi kapena wamwamuna M'nyumba ya Yehova Mulungu
wanu kudzapereka za malumbiro aliwonse, chifukwa Yehova Mulungu
wanu amadana ndi zimenezi.

19 Musamalipitse m'bale wanu chiwongoladzanja, kaya pa ndalama,
kapena pa chakudya, kapena pa china chilichonse choti n'kupereketsa chi-
wongoladzanja. 20 Mlendo mukhoza kumulipitsa chiwongoladzanja koma
osati m'bale wanu Mwisraeli, kuti Yehova Mulungu wanu akudalitseni pa
zochitika zanu zonse m'dziko mukulowamoli.

21 Mukalumbira kupereka kanthu kwa Yehova Mulungu wanu,
musamachedwetse kupereka, chifukwa Yehova Mulungu wanu adzaku-
funsanibe kanthuko ndipo mudzapezeka wochimwa. 22 Koma ngati
mupewa kupanga mapangano simudzapezeka ochimwa. 23 Zilizonse
zimene mulumbira ndi pakamwa panu muzitsimikiza kuzichita, chifukwa
mwalumbira mwaufulu pamaso pa Yehova Mulungu wanu ndi pakamwa
panu.

24 Mukalowa m'munda wamphesa wa mnzanu mukhoza kudya mphesa
mmene mungafunire koma musayike zina m'dengu mwanu. 25 Mukalowa
m'munda wa tirigu wa m'bale wanu, mukhoza kutengako ngala m'manja
mwanu, koma osasenga tirigu ndi chikwakwa.

# 24

1 Ngati mwamuna wakwatira mkazi amene sakukondwera naye chi-
fukwa wapeza vuto pa mkaziyo, namulembera mkaziyo kalata ya
chisudzulo, namupatsa ndi kumutulutsa m'nyumba mwake, 2 mkaziyo
ndi kukakwatiwa ndi mwamuna wina, 3 ndipo mwamuna wachi-
wiriyo n'kuyipidwa nayenso ndi kumulemberanso kalata ya chisudzulo
n'kumutulutsa m'nyumba mwake, kapena ngati mwamunayo amwalira,
4 mwamuna wake woyamba uja, amene anamuleka saloledwanso kumuk-
watira kachiwiri popeza mkaziyo wadetsedwa. Chimenechi ndi chonyansa
pamaso pa Yehova. Musalowetse tchimo m'dziko limene Yehova Mulungu
wanu akukupatsani ngati cholowa chanu.

5 Mwamuna akangokwatira kumene asamatumizidwe ku nkhondo
kapena kupatsidwa ntchito ina iliyonse. Kwa chaka chathunthu akhale
ndi ufulu wokhala pa khomo pake kumasangalatsa mkazi wakeyo.
6 Munthu akakhala nanu ndi ngongole musamutengere mwala wake
wa mphero ngati chikole, chifukwa kutero n'kumutengera moyo kukhala
chikole cha ngongole.
7 Ngati munthu agwidwa akuba m'bale wake wa Chiisraeli nama-
muzunza ngati kapolo kapena kumugulitsa, wogulitsa mnzakeyo ayenera
kuphedwa. Muyenera kuchotsa choyipa pakati panu.
8 Pakagwa matenda a khate, samalitsani kuchita zonse zimene ansembe,
amene ndi Alevi, anakulangizani. Mutsatire mosamalitsa zimene ndi-
nawalamula. 9 Kumbukirani zimene Yehova Mulungu wanu anachita kwa
Miriamu muli paulendo mutatuluka mu Igupto.
10 Ukabwereketsa mnzako kanthu kena kalikonse, usalowe m'nyumba
mwake kukatenga chimene wachipereka ngati chikole. 11 Uziyima kunja
kwa nyumba kuti munthu amene wamubwereketsa kanthuyo akubw-
eretsere kunja komweko. 12 Ngati munthuyo ndi wosauka, usamutengere
chikolecho mpaka kukagona nacho kwanu. 13 Pomalowa dzuwa ukhale
utamubwezera mkanjo wakewo kuti akafunde. Pamenepo adzakuthokoza,
ndipo amenewa adzawerengedwa ngati machitidwe olungama kwa iweyo
pamaso pa Yehova Mulungu wako.
14 Osamapezera mwayi pa anthu aganyu osauka ndi aumphawi, kaya
ndi Mwisraeli kapena mlendo wokhala mu umodzi mwa mizinda yanu.
15 Mumulipire malipiro ake a tsiku dzuwa lisanalowe chifukwa ndi
wosauka ndipo akudalira malipirowo. Kupanda kutero adzakudandauli-
rani kwa Yehova ndipo mudzapezeka ochimwa.
16 Makolo asaphedwe chifukwa cha ana awo, ndipo ana asaphedwe
chifukwa cha makolo awo, koma aliyense ayenera kufa chifukwa cha
zolakwa zake.
17 Musachitire mlendo kapena mwana wamasiye zoyipa, kapena
kulanda mkazi wamasiye chovala ngati chikole cha ngongole.
18 Kumbukirani kuti munali akapolo m'dziko la Igupto ndipo Yehova
Mulungu wanu anakuwombolani kumeneko. N'chifukwa chake
ndikukulamulani kuti muzichita zimenezi.
19 Mukamakolola m'munda mwanu ndipo zokolola zina zikasiyidwa,
musamabwerere kukazitola. Muzilekere alendo, ana ndi akazi amasiye,
kuti Yehova Mulungu wanu akudalitseni pa zochita zanu zonse.
20 Mukathyola zipatso mu mtengo wa olivi, musamabwerereenso kachiwiri
ku mtengo womwewo. Zotsalazo zilekereni alendo, ana ndi akazi
amasiye. 21 Mukakolola mphesa m'munda mwanu musamabwerere-
monso kachiwiri. Zotsalazo muzilekere alendo, ana ndi akazi amasiye.
22 Kumbukirani kuti munali akapolo m'dziko la Igupto. N'chifukwa chake
ndikukulamulani kuti muzichita zimenezi.

# 25

1 Anthu akasemphana mawu, ayenera kupita ku bwalo la milandu
ndipo woweruza adzaweruza mlanduwo. Adzamasula wosalakwa
nalanga wolakwa. 2 Munthu akapezeka wolakwa ayenera kukwapulidwa,
woweruza amugoneke pansi wolakwayo ndipo akwapulidwe pamaso pake
zikoti zochuluka molingana ndi mlandu wake, 3 koma asamukwapule
zikoti zopitirira makumi anayi. Akakwapulidwa kupitirira apo ndiye kuti
m'bale wanuyo anyozeka pamaso panu.

4 Musamange ng'ombe pakamwa pamene ikupuntha tirigu.

5 Ngati abale akukhala pamodzi ndipo wina mwa iwo akamwalira
wosasiya mwana wamwamuna, mkazi wamasiyeyo asakakwatiwe ndi
mlendo. M'bale wake wa mwamuna wakeyo amukwatire kukwaniritsa
chimene akuyenera kuchita kwa mlamu wakeyo. 6 Mwana wamwamuna
woyamba amene mayiyo angabereke ayenera kutenga dzina la mwamuna
wake womwalirayo kuti dzina lake lisafafanizike mu Israeli.

7 Komabe, ngati munthu sakufuna kukwatira mkazi wa m'bale wakeyo,
mkaziyo ayenera kupita kwa akuluakulu ku chipata cha mzinda ndi
kukanena kuti, "M'bale wake wa mwamuna wanga akukana kupitiriza
dzina la m'bale wake mu Israeli. Iye akukana kulowa chokolo."
8 Pamenepo akuluakulu a mu mzinda wawowo adzamuyitanitsa nakamba
naye. Ngati alimbikirabe kunena kuti, "Ine sindikufuna kumukwatira
mkaziyu," 9 mkazi wamasiye wa m'bale wakeyo adzapita kwa iye
pamaso pa akuluakuluwo namuvula nsapato imodzi, adzamulavulire
kumaso n'kunena kuti, "Izi ndi zimene amachitira munthu amene safuna
kupitiriza mbiri ya banja la m'bale wake." 10 Mbiri ya banja la munthu
ameneyo idzadziwika mu Israeli kuti ndi Banja la Wovulidwa nsapato.

11 Ngati anthu awiri akuchita ndewu ndipo mkazi wa mmodzi wa iwo
abwera kudzaleretsa mwamuna wake kwa mnzakeyo natambasula dzanja
lake kugwira ku maliseche kwa winayo, 12 muyenera kumudula dzanja,
osamumvera chisoni.

13 Musamakhale ndi miyeso iwiri yosiyana m'thumba mwanu, wole-
mera ndi wopepuka. 14 Musamakhale ndi milingo iwiri yosiyana
m'nyumba mwanu, waukulu ndi waung'ono. 15 Muyenera kukhala ndi
miyeso ndi milingo yoyenera ndi yosanyenga kuti mukhalitse m'dziko
limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani. 16 Pakuti Yehova Mulungu
wanu amanyansidwa ndi aliyense wochita za chinyengo zoterezi.

17 Kumbukirani zimene Aamaleki anakuchitirani pamene munali pa
ulendo wochokera ku Igupto. 18 Pamene munali otopa ndi ofowoka,
iwo anakumana nanu pa ulendo wanu ndi kukantha onse otsalira
m'mbuyo ndipo iwo sanaope Mulungu. 19 Pamene Yehova Mulungu
wanu akupumulitsani kwa adani onse okuzungulirani m'dziko limene
akupatsani inu ngati cholowa chanu, mudzawafafanize Aamaleki, asadza-
wakumbukirenso pa dziko lapansi. Musadzayiwale chimenechi!

# 26

*Zipatso Zoyamba ndi Chakhumi*

1 Mukalowa ndi kukhazikika m'dziko limene Yehova Mulungu wanu
akukupatsani ngati cholowa chanu, 2 mutengeko zina mwa zipatso
zoyamba pa zonse zimene mudzakola m'nthaka ya dziko limene Yehova
Mulungu wanu akukupatsani ndi kuziyika m'dengu. Mukatero mupite
kumalo kumene Yehova Mulungu wanu adzakhazikitsako dzina lake
3 ndipo mudzamuwuze wansembe amene ali pa ntchito pa nthawiyo
kuti, "Ndikunenetsa lero kwa Yehova Mulungu wanu kuti ndabwera ku
dziko limene Yehova analumbirira makolo athu kuti adzatipatsa ife."
4 Wansembe adzatenga dengulo m'manja mwanu ndi kuliyika pansi patso-
golo pa guwa lansembe la Yehova Mulungu wanu. 5 Ndipo mudzanenetsa
pamaso pa Yehova Mulungu wanu kuti, "Abambo anga anali Mwaramu
woyendayenda, anapita ku Igupto ndi anthu ochepa nakhala kumeneko.

Pambuyo pake anakhala mtundu waukulu, wamphamvu ndi wochu-
luka. 6 Koma Aigupto anatisautsa natizunza, kumatigwiritsa ntchito
yakalavulagaga. 7 Kenaka tinafuwulira Yehova, Mulungu wa makolo
athu ndipo Yehova anamva mawu athu ndi kuona kusauka, kuvutika ndi
kuponderezedwa kwathu. 8 Kotero Yehova anatitulutsa ku Igupto ndi
dzanja lake lamphamvu ndi mkono wotambasuka ndi zoopsa zazikulu
ndi zizindikiro zozizwitsa ndi zodabwitsa. 9 Iye anatibweretsa ku malo
ano natipatsa dziko loyenda mkaka ndi uchi lino. 10 Ndipo tsopano
ndikubweretsa zipatso zoyamba zimene inu Yehova mwandipatsa.” Ikani
dengulo pamaso pa Yehova Mulungu wanu ndi kuwerama mopereka
ulemu pamaso pake. 11 Ndipo inu ndi Alevi pamodzi ndi alendo okhala
pakati panu mudzakondwera m'zinthu zonse zabwino zimene Yehova
Mulungu wanu wakupatsani, inu ndi a pa banja panu.

12 Mukatha kupatula chakhumi pa zonse zimene mwakolola m'chaka
chachitatu chimene ndi chaka chakhumi, muzichipereka kwa wansembe,
mlendo, ana ndi akazi amasiye, kuti pamenepo adye m'mizinda yanu
nakhuta. 13 Kenaka munene kwa Yehova Mulungu wanu kuti “Ndatulut-
samo m'nyumba mwanga gawo lopatulika ndipo ndalipereka kwa Mlevi,
mlendo, ana ndi akazi amasiye, monga mwa zonse zimene munalamula.
Sindinapatuke pa zimene munalamula kapena kuyiwala ndi chimodzi
chomwe. 14 Sindinadye kalikonse ka gawo lopatulika pamene ndimalira
maliro kapena kuchotsapo kalikonse ka gawo lopatulika pamene ndinali
wodetsedwa, kapena kuperekako nsembe kwa akufa kalikonse ka gawoli.
Ine ndamvera Yehova Mulungu wanga, ndachita chilichonse chimene
inu munandilamula. 15 Yang'anani pa dziko kuchokera kumwamba, ku
malo anu wopatulika, ndi kudalitsa anthu anu Aisraeli ndi dziko loyenda
mkaka ndi uchi limene mwatipatsa ife monga momwe munalonjezera pa
malumbiro anu kwa makolo athu.”

### *Tsatirani Malamulo a Yehova*

16 Yehova Mulungu wanu akukulamulani lero lino kuti mutsate malan-
gizo ndi malamulo ake ndipo muwasunge mosamalitsa ndi mtima wanu
wonse ndi moyo wanu wonse. 17 Mwanena motsimikiza lero lino
kuti Yehova ndiye Mulungu wanu ndi kuti mudzayenda m'njira zake,
kusunga malangizo, malamulo ndi zonse akukulamulani ndi kutinso
mudzamumvera. 18 Ndipo Yehova wanenetsa lero lino kuti inu ndinu
anthu ake, chuma chake chamtengowapatali monga momwe analonjezera,
ndipo mukuyenera kusunga malamulo ake onse. 19 Iye wanenetsa
kuti adzakuyikani kukhala oyamikika, otchuka ndi olemekezeka koposa
mitundu yonse imene anayilenga. Komanso mudzakhala anthu opatulika
a Yehova Mulungu wanu monga momwe analonjezera.

## 27

### *Guwa Lansembe ku Phiri la Ebala*

1 Mose ndi akuluakulu a Israeli analamula anthu kuti, “Sungani
malamulo onse amene ndikukupatsani lero lino. 2 Mukawoloka mtsinje
wa Yorodani kulowa m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani,
muyimiritse miyala ingapo ikuluikulu ndi kuyikulungiza. 3 Mulembepo
mawu onse a malamulo amenewa pamene muwoloka kulowa m'dziko
limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani, dziko loyenda mkaka ndi
uchi, monga momwe Yehova Mulungu wa makolo anu anakulonjez-
erani. 4 Ndipo mukawoloka Yorodani muyimike miyala iyi pa Phiri la

Ebala monga momwe ndikukulamulirani lero lino ndipo muyikulungize.
5 Pamenepo mumange guwa lansembe la miyala la Yehova Mulungu
wanu. Musagwiritse ntchito chida chilichonse chachitsulo pa miyalapo.
6 Mumange guwa lansembe la Yehova Mulungu wanu ndi miyala
yakutchire ndi kuperekerapo nsembe yopsereza kwa Yehova Mulungu
wanu. 7 Muperekerepo nsembe zopereka za chiyanjano, muzidye ndi
kukondwera pamaso pa Yehova Mulungu wanu. 8 Ndipo pa miyalapo
mudzalembepo mawu onse a malamulo ndi malemba akuluakulu."

### *Matemberero Kuchokera ku Phiri la Ebala*

9 Kenaka Mose ndi ansembe, amene ndi Alevi anati kwa Aisraeli onse, "Khalani chete Aisraeli inu ndipo mumvetsere! Tsopano inu ndinu anthu a Yehova Mulungu wanu. 10 Muzimvera Yehova Mulungu wanu ndi kutsata malamulo ake ndi malangizo ake omwe ndikukupatsani lero lino."

11 Tsiku lomwelo Mose analamula anthu kuti:

12 Mukawoloka Yorodani, mafuko awa akayimirire pa Phiri la Gerizimu ndi kudalitsa anthu: Simeoni, Levi, Yuda, Isakara, Yosefe ndi Benjamini.
13 Ndipo mafuko awa akayimirire pa Phiri la Ebala ndi kutchula matemberero: Rubeni, Gadi, Aseri, Zebuloni, Dani ndi Nafutali.

14 Alevi adzayankhula mokweza kwa Aisraeli onse kuti:

15 "Ndi wotembereredwa munthu amene asema chifanizo kapena kupanga fano, ndi kuchiyika mobisa, pakuti chimenechi ndi chinthu chodetsedwa pamaso pa Yehova, ntchito za manja a anthu."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

16 "Ndi wotembereredwa munthu amene sachitira ulemu abambo ake kapena amayi ake."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

17 "Ndi wotembereredwa munthu amene amasuntha mwala wa malire wa mnzake."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

18 "Ndi wotembereredwa munthu amene amasocheretsa munthu wosaona pa msewu."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

19 "Ndi wotembereredwa munthu amene sachitira chilungamo mlendo, ana amasiye kapena mkazi wamasiye."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

20 "Ndi wotembereredwa munthu amene agonana ndi mkazi wa abambo ake pakuti iye sachitira ulemu pogona pa abambo ake."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

21 "Ndi wotembereredwa munthu amene achita chigololo ndi nyama ya mtundu uli wonse."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

22 "Ndi wotembereredwa munthu amene agonana ndi mlongo wake, mwana wamkazi wa abambo ake kapena mwana wamkazi wa amayi ake."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

23 "Ndi wotembereredwa munthu amene agonana ndi apongozi ake."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

24 "Ndi wotembereredwa munthu amene apha mnzake mwachinsinsi."

Pamenepo anthu onse adzati, "Ameni!"

25 “Ndi wotembereredwa munthu amene alandira chiphuphu kuti aphe munthu wosalakwa.”

Pamenepo anthu onse adzati, “Ameni!”

26 “Ndi wotembereredwa aliyense amene sachita kapena sasunga mawu a malamulo awa.”

Pamenepo anthu onse adzati, “Ameni!”

# 28

*Madalitso Akumvera*

1 Ngati mumvera Yehova Mulungu wanu ndi kutsatira mosamalitsa
malamulo ake onse amene ndikukupatsani lero lino, Yehova Mulungu
wanu adzakukwezani pamwamba pa mitundu yonse ya pa dziko lapansi.
2 Madalitso awa adzabwera kwa inu ndi kuyenda nanu ngati mumvera
Yehova Mulungu wanu:

3 Mudzadalitsika m’mizinda yanu ndi kudalitsika m’dzikolo.

4 Yehova adzadalitsa ana anu, zokolola za m’dziko lanu, ng’ombe zanu pamodzi ndi ziweto zanu zonse.

5 Dengu lanu ndi chiwaya chanu cha buledi zidzadalitsika.

6 Mudzadalitsika pa kulowa kwanu ndi pa kutuluka kwanu.

7 Yehova adzaonetsetsa kuti adani anu amene adzakuwukirani agonjetsedwe pamaso panu. Iwo adzabwera kwa inu kuchokera mbali imodzi koma adzakuthawani ku mbali zisanu ndi ziwiri.

8 Yehova adzatumiza madalitso pa nkhokwe zanu ndi pa chilichonse chimene muchikhudza. Yehova Mulungu wanu adzakudalitsani m’dziko limene akukupatsani.

9 Yehova Mulungu wanu adzachititsa kuti mukhale anthu ake opatulika,
monga momwe analonjezera pa malumbiro ake, ngati musunga malamulo
ake ndi kuyenda m’njira zake. 10 Pamenepo anthu onse a dziko lapansi
adzaona kuti mumadziwika ndi dzina la Yehova ndipo adzakuopani.
11 Yehova adzakupambanitsani kwambiri ndipo adzakupatsani ana ambiri,
ziweto zambiri, ndi zokolola zochuluka, m’dziko limene Yehova
analumbira kwa makolo anu kuti adzakupatsani.

12 Yehova adzatsekula kumwamba kumene amasungirako chuma chake,
kutumiza mvula m’dziko lanu pa nthawi yake ndi kudalitsa ntchito yonse
ya manja anu. Mudzakongoza mitundu yambiri koma inu simudzakongola
kwa aliyense. 13 Yehova adzakuthandizani kukhala mutu osati mchira.
Mukakhala ndi chidwi ndi malamulo a Yehova Mulungu wanu amene
ndikukupatsani lero lino ndi kuwatsata mosamalitsa, inu mudzakhala
apamwamba nthawi zonse osati apansi. 14 Musapatukire ku dzanja
lamanja kapena lamanzere pa lamulo lina lililonse limene ndikukupatsani
lero lino ndi kumatsatira kapena kuyitumikira milungu ina.

*Matemberero Akusamvera*

15 Koma ngati simumvera Yehova Mulungu wanu ndi kusatsata mosamalitsa malamulo ake ndi malangizo ake onse amene ndikukupatsani lero lino, matemberero awa adzabwera pa inu ndikukugonjetsani:

16 Mudzatembereredwa mu mzinda ndi kutembereredwa m’mudzi.

17 Dengu lanu ndi chiwaya chanu cha buledi zidzatembereredwa.

18 Zipatso za m’mimba mwanu zidzatembereredwa, ndiponso zomera za m’dziko lanu, ana ang’ombe zanu ndi ana ankhosa zanu zidzatembereredwa.

19 Mudzatembereredwa pa kulowa kwanu ndi pa kutuluka kwanu.

20 Yehova adzakutumizirani matemberero, chisokonezo ndi minyozo
pa chilichonse chimene mudzachichita mpaka mudzawonongedwa ndi
kukhala bwinja mofulumira chifukwa cha zoyipa zimene mwazichita pa
kumutaya Yehova. 21 Yehova adzakugwetserani mliri wa matenda mpaka
atakuwonongani m'dziko limene mukulowa kukalitengali. 22 Yehova
adzakukanthani ndi nthenda yowondetsa, ya malungo ndi ya zotupatupa,
ndi kutentha kwakukulu ndi chilala, ndi chinsikwi ndi chiwawu zimene
zidzakusautsani mpaka mutawononGeka. 23 Mitambo ya pamutu panu
idzawuma ngati mkuwa ndipo sidzagwetsa mvula mpaka nthaka yanu
idzawuma gwaa ngati chitsulo. 24 M'malo mwa mvula Yehova adzakupat-
sani fumbi ndi dothi ndipo lidzakugwerani kuchokera kumwamba mpaka
mutawonongeka.

25 Yehova adzalola kuti adani anu akugonjetseni. Mudzadzera njira
imodzi pokalimbana ndi adani anu koma pothawa mudzabalalika mbali
zisanu ndi ziwiri. Mudzakhala chinthu chochititsa mantha pakati pa
maufumu onse a dziko lapansi. 26 Mitembo yanu idzadyedwa ndi
mbalame zamumlengalenga ndi nyama zakutchire, ndipo palibe amene
adzaziyingitse. 27 Yehova adzakusautsani ndi zithupsa za ku Igupto ndi
zotupatupa, zipere, ndi mphere zimene simudzachiritsika nazo. 28 Yehova
adzakusautsani inu ndi misala, khungu ndi chisokonekero cha maganizo.
29 Masanasana mudzayenda ngati muli mu mdima, kumafufuzira njira
ngati wosaona. Mudzakhala olephera pa chilichonse mungachite. Tsiku
ndi tsiku mudzaponderezedwa ndi kuberedwa wopanda wokupulumut-
sani.

30 Mudzachita chinkhoswe ndi mkazi, koma wina adzakulandani ndi
kumukwatira. Mudzamanga nyumba koma simudzagonamo. Mudzalima
munda wamphesa koma simudzadyako zipatso zake. 31 Ng'ombe yanu
yamtheno idzaphedwa inu muli pomwepo koma simudzadyako. Bulu
wanu adzalandidwa kwa inu mwamakani osabwera nayenso. Nkhosa
zanu zidzapatsidwa kwa adani anu, ndipo palibe amene adzazipulumutsa.
32 Ana anu aamuna ndi aakazi adzaperekedwa kwa anthu a mitundu
ina ndipo inu mudzafika potopa ndi kulefuka n'kudikirira tsiku ndi
tsiku kuti mwina anawo abwerako. 33 Anthu amene simukuwadziwa
adzakudyerani zokolola zanu, ndipo mudzakhala mukuponderezedwa
mwankhanza masiku onse. 34 Zimene muzidzaziona zidzakusokonezani
mitu. 35 Yehova adzakusautsani ndi zithupsa zaululu ndi zosachiritsika za
m'mawondo ndi m'miyendo ndipo zidzafalikira kuchoka kuphazi mpaka
kumutu.

36 Yehova adzakuthamangitsirani, inu ndi mafumu anu amene
muwayika, ku dziko losadziwika kwa inu ndi kwa makolo anu. Kumeneko
mudzakapembedza milungu ina, milungu ya mitengo ndi miyala. 37 Inu
mudzakhala chinthu chochititsa mantha kuchisunga ndiponso chinthu
chotukwanidwa ndi chonyozeka kwa anthu a mitundu yonse kumene
Yehova adzakuthamangitsirani.

38 Mudzadzala mbewu zambiri ku munda koma mudzakolola pang'ono,
chifukwa dzombe lidzaziwononga. 39 Mudzadzala mpesa ndi kulimirira
koma vinyo wake simudzamumwa kapena kukolola mphesazo, chifukwa
mphutsi zidzadya mphesazo. 40 Mudzakhala ndi mitengo ya olivi m'dziko
lanu lonse koma simudzagwiritsa ntchito mafuta ake, chifukwa zipatso
zake zidzayoyoka. 41 Mudzabereka ana aamuna ndi aakazi koma

sadzakhala anu, chifukwa adzapita ku ukapolo. 42 Magulumagulu a
dzombe adzawononga mitengo yanu ndi mbewu za m'dziko lanu.

43 Mlendo wokhala pakati panu adzatukuka kuposa inu, koma in-
uyo mudzaloweralowera pansi. 44 Iye adzakubwereketsani, koma inu
simudzatha kubwereketsa. Iye adzakhala mutu ndipo inu mudzakhala
mchira.

45 Matemberero onsewa adzabwera pa inu. Adzakulondolani ndi
kukugonjetsani mpaka mutawonongeka, chifukwa simunamvere Yehova
Mulungu wanu ndi kusunga malamulo ndi malangizo amene anakupat-
sani. 46 Matemberero amenewa adzakhala chizindikiro ndi chozizwitsa
kwa inu ndi zidzukulu zanu mpaka kalekale. 47 Pakuti inu simunatumikire
Yehova Mulungu wanu pa nthawi imene zinthu zinkakuyenderani bwino,
48 chomwecho pa nthawi ya njala ndi ludzu, ya maliseche ndi umphawi
woopsa, mudzatumikira adani amene Yehova adzakutumizirani. Iye
adzayika goli lachitsulo m'khosi mwanu kufikira atakuwonongani.

49 Yehova adzakutumizirani mtundu wa anthu kuchokera kutali
kumapeto kwa dziko lapansi nudzachita ngati mphungu yowulukira pansi,
mtundu wa anthu umene chiyankhulo chawo simudzachimva, 50 mtundu
wooneka wochititsa mantha, wopanda ulemu kwa okalamba kapena
chisoni kwa ana. 51 Iwo adzagwira ana a ziweto zanu, natenga zokolola za
m'dziko lanu kufikira mutawonongeka. Iwo sadzakusiyirani tirigu, vinyo
watsopano kapena mafuta a olivi, kapena mwana wang'ombe aliyense
kapena mwana wankhosa mpaka mutasanduka bwinja. 52 Iwo adzathira
nkhondo mizinda yonse m'dziko lanu lonse mpaka malinga anu ataliatali
omwe mumadalira aja atagwa. Adzathira nkhondo mizinda yonse ya
m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akukupatsani.

53 Chifukwa cha zosautsa zimene mdani wanu adzabweretsa pa nthawi
yokuthirani nkhondo, inu mudzadya ana anu, mnofu wa ana anu aamuna
ndi aakazi amene Yehova Mulungu wanu wakupatsani. 54 Ngakhale
munthu woleza mtima ndi wachifundo kwambiri pakati panu sadzakhala
ndi chifundo pa m'bale wake weniweni kapena mkazi wake amene iye
amamukonda kapena ana ake otsalawo, 55 ndipo sadzagawirako aliyense
wa iwo mnofu wa ana ake amene akudyawo. Kadzakhala kali komweko
basi kamene kamutsalira chifukwa cha msautso umene mdani wanu adza-
gwetsa pa nthawi yothira nkhondo mizinda yanu yonse. 56 Mayi woleza
mtima ndi wachifundo kwambiri pakati panu, uja woti sangayerekeze
kuponda pansi, adzabisira mwamuna wake amene amamukonda ndi ana
ake omwe aamuna ndi aakazi 57 zotsalira za uchembere zochoka m'mimba
mwake ndi ana amene wabereka. Pakuti adzafuna kuti adye zimenezi
yekha mobisa pa nthawi yothiridwa nkhondo chifukwa cha masautso
amene mdani wanu adzagwetsa pa inu m'mizinda yanu.

58 Ngati simutsata mosamalitsa mawu onse a malamulo awa amene
alembedwa m'buku lino, komanso ngati simuopa dzina la ulemerero
ndi loopsa, dzina la Yehova Mulungu wanu, 59 Yehova adzatumiza pa
inu ndi zidzukulu zanu miliri yoopsa, zosautsa zowawa ndi zokhalitsa,
ndi matenda aakulu ndi ovuta kuchiritsika. 60 Adzakubweretserani
matenda onse a ku Igupto aja mumawaopawa ndipo adzakukanirirani.
61 Yehova adzakubweretseraninso mtundu uliwonse wa matenda ndi
zosautsa zimene sizinalembedwe m'buku la malamulo lino, mpaka
mutawonongeka. 62 Inu aja munali ochuluka ngati nyenyezi zakumwamba
mudzatsala ochepa chabe chifukwa simunamvere Yehova Mulungu wanu.

63 Monga kunamukomera Yehova kukulemeretsani ndi kukuchulukitsani,
momwemonso kudzamukondweretsa kukunthani ndi kukuwonongani.
Inu mudzazulidwa kukuchotsani m'dziko limene mukulowa kukalitengali.

64 Kenaka Yehova adzakubalalitsani pakati pa anthu a mitundu yonse,
kuchokera ku mapeto a dziko kufika ku mapeto ena. Kumeneko
mudzapembedza milungu ina, milungu ya mitengo ndi ya miyala, imene
inu eni kapena makolo anu sanayidziwepo. 65 Pakati pa mitundu
ya anthu imeneyi simudzapeza mpata, popanda malo woti n'kuyikapo
phazi. Kumeneko Yehova adzakupatsani moyo wa nkhawa, maso
otopa ndi chiyembekezo, ndi mtima wosakhazikika. 66 Inu mudzakhala
osakhazikika mopitirira, odzazidwa ndi mantha usiku ndi usana womwe,
osowa chitsimikizo cha pa moyo wanu. 67 Mmawa muzidzati, "Chikhala
anali madzulo!" ndipo madzulo mudzati, "Chikhala unali mmawa!"
Mudzanena zimenezi chifukwa cha mantha amene adzakhale mu mtima
mwanu ndi chifukwa cha zomwe muzidzaziona. 68 Yehova adzakubwezani
ku Igupto pa sitima zapamadzi paulendo umene Ine ndinati musawuyen-
denso. Kumeneko mudzadzitsatsa nokha kwa adani anu monga akapolo
aamuna ndi aakazi, koma palibe amene adzakuguleni.

# 29

*Kukonzanso Pangano*

1 Awa ndiwo mawu a m'pangano limene Yehova analamula Mose
kuti achite ndi Aisraeli ku Mowabu, powonjezera pa pangano limene
anapangana nawo ku Horebu.

2 Mose anayitanitsa Aisraeli onse nati kwa iwo:

Inu munaona zonse zimene Yehova anachita kwa Farao, nduna zake
ndi dziko lake lonse ku Igupto. 3 Ndi maso anu munaona mayesero onse
aja, zizindikiro zozizwitsa ndi zodabwitsa zazikulu zija. 4 Koma mpaka
lero Yehova sanakupatseni mtima wozindikira kapena maso openya
kapena makutu akumva. 5 M'zaka makumi anayi zimene ndinakutso-
golerani m'chipululu, zovala zanu ndiponso nsapato za ku mapazi anu
sizinang'ambike. 6 Inu simunadye buledi ndi kumwa vinyo kapena
chakumwa chilichonse choledzeretsa. Ndinachita izi kuti mudziwe kuti
Ine ndine Yehova Mulungu wanu.

7 Pamene munafika malo ano, Sihoni mfumu ya ku Hesiboni ndi Ogi
mfumu ya ku Basani anabwera kudzamenyana nafe koma tinawagonjetsa
iwo. 8 Tinatenga dziko lawo ndi kulipereka ngati cholowa cha fuko la
Rubeni, fuko la Gadi ndi theka la fuko la Manase.

9 Tsatirani mosamalitsa mawu a m'pangano ili kuti zinthu zizikuyen-
derani bwino pa zochitika zanu zonse. 10 Lero lino nonse mukuyima pa-
maso pa Yehova Mulungu wanu, atsogoleri a mafuko anu, akuluakulu ndi
nduna zanu, ndi amuna ena onse a mu Israeli, 11 pamodzi ndi ana ndi akazi
anu, kudzanso alendo amene akukhala pakati panu omwe amakuwazirani
nkhuni ndi kukutungirani madzi. 12 Mukuyimirira pano kuti mulowe
m'pangano ndi Yehova Mulungu wanu, pangano limene Yehova akuchita
ndi inu lero ndi kulisindikiza ndi malumbiro, 13 kukukhazikitsani lero lino
ngati anthu ake, ndi kuti Iye akhale Mulungu wanu monga anakulonjezani
inu ndiponso monga analumbira kwa makolo anu Abrahamu, Isake ndi
Yakobo. 14 Ndikupanga pangano ili ndi malumbiro ake osati kwa inu

nokha, 15 amene muli pano pamaso pa Yehova Mulungu wathu, koma ndi
iwonso amene sali pano lero.

16 Inu nomwe mukudziwa mmene tinkakhalira ku Igupto ndi mmene
tinadutsira mayiko pa ulendo wobwera kuno. 17 Ife tinaona pakati
pawo mafanizo ndi mafano awo onyansa, amtengo ndi amiyala, asiliva
ndi agolide. 18 Onetsetsani kuti pasapezeke mwamuna kapena mkazi,
banja kapena fuko pakati panu lero amene mtima wawo udzapandukira
Yehova Mulungu wanu ndi kupita kukapembedza milungu ya mitundu
iyo. Onetsetsani kuti pasapezeke muzu pakati panu wotulutsa mankhwala
akupha otere.

19 Munthu wotere akamva mawu a lumbiro ili, asadzidalitse yekha
m'maganizo mwake namati, "Ine ndidzapulumuka ngakhale nditapitiriza
kuyenda njira yanga." Zoterezi zidzadzetsa masautso pa nthaka ya
chinyontho ndi yowuma yomwe. 20 Yehova sadzamukhululukira. Mkwiyo
ndi nsanje ya Yehova zidzamuyakira munthuyo. Matemberero onse
wolembedwa m'bukuli adzamugwera iye ndipo Yehova adzafafaniza
dzina lake pa dziko lapansi. 21 Yehova adzasankha pakati pa Aisraeli
anthu oyenera masautso monga mwa matemberero onse a m'pangano
olembedwa M'buku la Malamulo.

22 Ana anu a mibado yakutsogolo ndi alendo amene adzachokera
kutali adzaona matsoka amene adzakugwerani m'dziko muno ndiponso
matenda amene Yehova adzabweretsa pa dzikoli. 23 Dziko lonse lidza-
sanduka nthaka ya mchere ndi ya sulufule. Simudzadzalamo kanthu,
simudzakhala chomera chilichonse, ndi mbewu yomera m'menemo.
Dziko lanu lidzakhala lowonongeka ngati Sodomu ndi Gomora, Adima
ndi Zeboimu, mizinda imene Yehova anayiwononga ndi mkwiyo wake
waukulu. 24 Mitundu yonse ya anthu idzafunsa kuti, "Kodi chifukwa
chiyani Yehova anachita zotere m'dziko lake? Kodi chifukwa chiyani
anaonetsa mkwiyo woopsa wotere?"

25 Ndipo yankho la mafunso amenewa lidzakhala lakuti, "Chifukwa
chakuti anthu awa aphwanya pangano la Yehova Mulungu wa makolo
awo, pangano limene Iye anapangana nawo pamene anawatulutsa ku
Igupto. 26 Iwo anachoka ndi kukatumikira milungu ina ndi kuyipembedza,
milungu imene sanayidziwe, milungu imene sanawapatse. 27 Choncho
Yehova anakwiyira dziko lino, kotero anabweretsa matemberero onse
amene analembedwa m'buku lino. 28 Ndi mkwiyo komanso ukali wake
woopsa Yehova anawazula m'dziko lawo ndi kuwaponyera m'dziko lina,
monga mmene zilili lero lino."

29 Zinsinsi ndi za Yehova Mulungu wathu koma zinthu zimene zaul-
ulidwa ndi zathu ndi ana athu kwamuyaya, kuti titsatire mawu onse a
m'malamulowa.

# 30

*Madalitso Akabwerera kwa Yehova*

1 Madalitso ndi matemberero awa onse amene ndawayika pamaso
panu akadzafika pa inu, inu n'kukumbukira kulikonse kumene Yehova
Mulungu wanu wakubalalitsirani pakati pa mitundu ya anthu, 2 ndipo inu
pamodzi ndi ana anu n'kudzatembenukira kwa Yehova Mulungu wanu ndi
kumumvera ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse molingana
ndi chilichonse chimene ndakulamulani lero lino, 3 pamenepo Yehova
Mulungu wanu adzakukhalitsani monga kale ndi kukuchitirani chifundo,

ndipo adzakusonkhanitsani kukuchotsani ku mitundu ina ya anthu
kumene anakubalalitsirani. 4 Ngakhale atakupirikitsirani ku malekezero
a dziko lapansi, adzakusonkhanitsani kuchokera kumeneko ndi kukub-
weretsaninso. 5 Adzakubweretsani ku dziko limene linali la makolo
anu, ndipo lidzakhala lanu. Iye adzakulemeretsani ndi kukuchulukitsani
kupambana makolo anu. 6 Yehova Mulungu wanu adzasintha mitima
yanu pamodzi ndi mitima ya zidzukulu zanu, kotero kuti mudzamukonda
ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse, ndipo mudzakhala ndi
moyo. 7 Yehova Mulungu wanu adzayika matemberero awa onse pa
adani anu amene amadana nanu ndi kukuzunzani. 8 Inu mudzamveranso
Yehova ndi kutsatira malamulo ake onse amene ndikukupatsani lero
lino. 9 Pamenepo Yehova Mulungu wanu adzakulemeretsani pa zochita
zanu zonse ndipo adzakupatsani ana ambiri, zoweta zambiri, ndiponso
mudzakhala ndi zokolola zambiri za m'dziko lanu. Yehova adzakondwera
nanunso ndi kukulemeretsani monga momwe anakondwera ndi makolo
anu, 10 ngati mudzamvera Yehova Mulungu wanu ndi kusunga malamulo
ake ndi mawu ake amene alembedwa M'buku ili la Malamulo ndi
kutembenukira kwa Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse ndi
moyo wanu wonse.

### *Moyo kapena Imfa*

11 Tsopano zimene ndikukulamulirani leroli sizovuta kapena zapatali.
12 Sizili kumwamba, kuti muzichita kufunsa kuti, "Kodi ndani amene
akwere kumwamba kuti akazitenge ndi kudzatilalikira kuti timvere?"
13 Komanso sizili pa tsidya la nyanja, kuti muzichita kufunsa kuti, "Kodi
ndani amene adzawoloke nyanja kuti akatenge ndi kudzatilalikira kuti
timvere?" 14 Ayi, mawu ali pafupi ndi inu; ali m'kamwa mwanu ndi mu
mtima mwanu kuti muwamvere.

15 Taonani, lero ine ndayika pamaso panu moyo ndi zokoma, imfa ndi
chiwonongeko. 16 Pakuti lero ndikukulamulani kuti mukonde Yehova
Mulungu wanu, kuti muyende m'njira zake, ndi kusunga malamulo
ake, malangizo ake. Mukatero mudzakhala ndi moyo ndi kuchulukana,
ndipo Yehova Mulungu wanu adzakudalitsani m'dziko limene mukulowa
kukakhalamo.

17 Koma ngati mtima wanu udzatembenuka, inu n'kukhala
osandimvera, ndipo ngati mudzatengeka ndi kupita kukagwadira
milungu ina ndi kuyipembedza, 18 lero ndikulengeza kwa inu kuti
mudzawonongeka ndithu. Simudzakhala nthawi yayitali m'dziko limene
mukulowamo pamene mukuwoloka Yorodani kuti mulitenge.

19 Lero kumwamba ndi dziko lapansi zikhale mboni zodzakutsutsani
pakuti ndayika pamaso panu moyo ndi imfa, madalitso ndi matem-
berero. Tsopano sankhani moyo kuti inu ndi ana anu mukhale ndi
moyo. 20 Ndi kuti mukonde Yehova Mulungu wanu, kumvera mawu ake,
ndi kukhulupirika kwa Iye. Pakuti Yehova ndiye moyo wanu, ndipo
mudzakhala zaka zambiri m'dziko limene analumbira kulipereka kwa
makolo anu, Abrahamu, Isake ndi Yakobo.

## 31

### *Yoswa Alowa M'malo mwa Mose*

1 Tsono Mose anapita ndi kukayankhula mawu awa kwa Aisraeli
onse: 2 "Tsopano ndili ndi zaka 120, ndipo sindingathenso kukutsogol-
erani. Yehova wandiwuza kuti, 'Iwe sudzawoloka Yorodani.' 3 Mwini

wake Yehova Mulungu wanu ndiye amene adzakutsogolerani powoloka.
Iye adzawononga mitundu ina yonse, ndipo inu mudzatenga dziko
lawo. Yoswa adzakutsogoleraninso powoloka, monga momwe ananenera
Yehova. 4 Ndipo Yehova adzawawononga iwo monga momwe ana-
wonongera Sihoni ndi Ogi, mafumu Aamori, amene Iye anawawononga
pamodzi ndi dziko lawo. 5 Ambuye adzawapereka kwa inu, ndipo inu
mukawachitire zonse zimene ndakulamulani. 6 Khalani amphamvu ndi
olimba mtima. Musachite nawo mantha kapena kunjenjemera pamaso
pawo, chifukwa Yehova Mulungu wanu apita nanu. Sadzakusiyani kapena
kukutayani."

7 Pamenepo Yehova anayitana Yoswa pamaso pa Aisraeli onse ndipo
anamuwuza kuti, "Khala wamphamvu ndi wolimba mtima, pakuti iwe
udzatsogolera anthu awa ku dziko limene Yehova analumbira kulipereka
kwa makolo awo, ndipo iwe ukaligawe pakati pawo kuti likakhale cholowa
chawo. 8 Yehova mwini ndiye akukutsogolerani ndipo adzakhala nanu.
Sadzakusiyani kapena kukutayani. Usachite mantha ndiponso usataye
mtima."

### *Kuwerenga Malamulo*

9 Choncho Mose analemba malamulo awa nawapereka kwa ansembe,
ana Alevi, amene amanyamula Bokosi la Chipangano la Yehova, ndiponso
kwa akuluakulu onse a Aisraeli. 10 Kenaka Mose anawalamula kuti,
"Pamapeto pa zaka zisanu ndi ziwiri zilizonse, chaka cha kukhulu-
lukidwa ngongole, pa nthawi ya Chikondwerero cha Misasa, 11 pamene
Aisraeli onse abwera kudzaonekera pamaso pa Yehova Mulungu wanu
pamalo pamene Iye adzasankhe, mudzawerenge malamulo onsewa iwo
akumva. 12 Mudzasonkhanitse anthu onse pamodzi, amuna, akazi ndi ana
pamodzi ndi alendo amene akukhala m'mizinda yanu, kuti adzawamve
ndi kuphunzira kuopa Yehova Mulungu wanu ndi kutsatira mosamala
mawu onse a m'malamulowa. 13 Ana awo amene sadziwa malamulo
awa, ayenera kuwamva ndi kuphunzira kuopa Yehova Mulungu wanu
nthawi zonse pamene mukukhala m'dziko limene mukuwoloka Yorodani
kukalitenga."

### *Aneneratu za Kuwukira kwa Aisraeli*

14 Yehova anawuza Mose kuti, "Nthawi ya kufa kwako yafika. Itana
Yoswa ndipo mubwere ku tenti ya msonkhano, kumene Ine ndidzamulan-
giza." Choncho Mose ndi Yoswa anabwera ku tenti ya msonkhano.

15 Pamenepo Yehova anaonekera ku tenti m'chipilala cha mtambo, ndipo
mtambowo unayima pamwamba pa khomo lolowera mu tenti. 16 Ndipo
Yehova anawuza Mose kuti, "Iwe ukupita kukapuma kumene kuli makolo
ako, ndipo ukangomwalira, anthu awa adzayamba kupembedza milungu
yachilendo ya m'dziko limene akukalowamo. Adzanditaya ndi kuphwanya
pangano lomwe ndinachita nawo. 17 Tsiku limenelo Ine ndidzawakwiyira
ndi kuwataya. Ndidzawabisira nkhope yanga, ndipo adzawonongedwa.
Masautso ambiri ndi zovuta zambiri zidzawagwera, ndipo tsiku limenelo
adzafunsa kuti, 'Kodi masautso awa sanagwere ife chifukwa Yehova
Mulungu wathu sali nafe?' 18 Ndipo Ine ndidzabisa ndithu nkhope yanga
pa tsiku limenelo chifukwa cha zoyipa zimene anachita potembenukira
kwa milungu ina.

19 "Tsopano ulembe mawu a nyimbo iyi ndipo uwaphunzitse Ais-
raeli, uwawuze kuti aziyimba, kuti ikhale mboni yanga yowatsutsa.
20 Pamene ndawalowetsa m'dziko loyenda mkaka ndi uchi, dziko limene

ndinalonjeza mwalumbiro kwa makolo awo, ndipo pamene adzadya
ndi kukhuta ndi kumasangalala, iwo adzatembenukira kwa milungu ina
ndi kumayipembedza, kundikana Ine ndi kuphwanya pangano langa.
21 Ndipo pamene masautso ambiri ndi zovuta zambiri zidzawagwera,
nyimbo iyi idzakhala mboni yanga yowatsutsa, chifukwa zidzukulu
zawo sizidzayiwala nyimboyi. Ine ndikudziwa zimene iwo akulingalira
kuchita, ngakhale kuti sindinawalowetse m'dziko limene ndinalonjeza
mwa lumbiro." 22 Choncho Mose analemba nyimbo iyi tsiku limenelo ndi
kuwaphunzitsa Aisraeli.

23 Yehova analamula Yoswa mwana wa Nuni kuti, "Khala wamphamvu
ndipo limba mtima, chifukwa udzalowetsa Aisraeli m'dziko limene
ndinawalonjeza mwa lumbiro, ndipo Ine mwini ndidzakhala nawe."

24 Mose atatha kulemba malamulowa m'buku, osasiyako kanthu,
25 analamula Alevi amene ananyamula Bokosi la Chipangano la Yehova
kuti, 26 "Tengani Buku ili la Malamulo ndi kuliyika pambali pa Bokosi
la Chipangano la Yehova Mulungu wanu. Likhale kumeneko ngati
mboni yokutsutsani. 27 Pakuti Ine ndikudziwa kuwukira kwanu ndi
kuwuma mtima kwanu. Ngati inu mwakhala mukuwukira Yehova ine
ndili moyo ndiponso ndili nanu pamodzi, nanga mudzawukira motani
ine ndikamwalira! 28 Mundisonkhanitsire atsogoleri onse a mafuko
anu pamodzi ndi akuluakulu onse, kuti ndiyankhule mawu awa iwo
akumva ndipo kumwamba ndi dziko lapansi zikhale mboni yowatsutsa.
29 Chifukwa ndikudziwa kuti ine ndikamwalira mudzayipa kwambiri
ndi kutembenuka kuleka njira imene ndinakulamulani. Masiku amene
akubwera, masautso adzakugwerani chifukwa mudzachita zoyipa pamaso
pa Yehova ndi kuputa mkwiyo wake chifukwa cha zimene manja anu
anapanga."

### *Nyimbo ya Mose*

30 Ndipo Mose ananena mawu a nyimbo iyi kuyiimba koyambira mpaka
potsiriza gulu lonse la Aisraeli likumva:

## 32

1 Mverani, inu mayiko a mmwamba ndipo ine ndidzayankhula;
imva, iwe dziko lapansi, mawu a pakamwa panga.
2 Chiphunzitso changa chigwe ngati mvula
ndipo mawu anga atsike ngati mame,
ngati mvumbi pa udzu watsopano,
ngati mvula yochuluka pa zomera zanthete.

3 Ndidzalalikira dzina la Yehova.
Aa, tamandani ukulu wa Mulungu wathu!
4 Iye ndi Thanthwe, ntchito zake ndi zangwiro,
njira zake zonse ndi zolungama.
Mulungu wokhulupirika amene salakwitsa,
Iye ndiye wolungama ndi wosalakwa.

5 Koma iwo achita mosakhulupirika pamaso pake,
iwo si ana akenso,
koma iwo ndi m'bado wachinyengo ndi wokhotakhota.
6 Kodi mukumubwezera Yehova chotere,
inu anthu opusa ndi opanda nzeru?

Kodi Iye si Atate anu, Mlengi wanu,
amene anakupangani ndi kukuwumbani?

7 Kumbukirani masiku amakedzana;
ganizirani za mibado yakalekale.
Funsa abambo ako ndipo adzakuwuza,
akuluakulu ako, ndipo adzakufotokozera.
8 Pamene Wammwambamwamba anapereka mayiko kwa anthu a mitundu ina kukhala cholowa chawo,
pamene analekanitsa anthu onse,
anayikira malire anthu onse
molingana ndi chiwerengero cha ana a Israeli.
9 Pakuti gawo la Yehova ndi anthu ake,
Yakobo ndiye cholowa chake.

10 Anamupeza m'chipululu,
ku malo owuma ndi kopanda kanthu.
Anamuteteza ndi kumusamalira;
anamutchinjiriza ngati mwanadiso wake,
11 ngati chiwombankhanga chimene chimasasula chisa chake
n'kumazungulira pamwamba pa ana ake,
chimene chimatambalalitsa mapiko ake kuti chigwire anawo
ndi kuwanyamula pa mapiko ake otambalalawo.
12 Yehova yekha ndiye anamutsogolera;
popanda thandizo la mulungu wachilendo.

13 Anamuyendetsa pamwamba pa mapiri a m'dziko
ndi kumudyetsa zipatso za m'minda.
Anamudyetsa uchi wofula pa thanthwe,
ndiponso mafuta ochokera m'nthaka ya miyala,
14 pamodzi ndi chambiko ndi mkaka wochokera ku ng'ombe ndi nkhosa,
ndiponso ana ankhosa onenepa ndi mbuzi,
pamodzinso ndi nkhosa zazimuna zabwino za ku Basani
ndiponso tirigu wabwino kwambiri.
Munamwa vinyo wa thovu lofiira.

15 Yesuruni ananenepa ndi kuyamba kuwukira;
atakhuta, ananenepa ndi kukula thupi.
Anasiya Mulungu amene anamulenga
ndipo anakana Thanthwe ndi Mpulumutsi wake.
16 Anamuchititsa nsanje ndi milungu yawo yachilendo
ndiponso anamukwiyitsa ndi mafano awo onyansa.
17 Anapereka nsembe kwa ziwanda zimene si Mulungu,
milungu imene sankayidziwa n'kale lomwe,
milungu yongobwera kumene,
milungu imene makolo anu sankayiopa.
18 Inu munasiya Thanthwe limene linakulerani;
munayiwala Mulungu amene anakubalani.

19 Yehova anaona zimenezi ndipo anawakana
chifukwa ana ake aamuna ndi aakazi anamukwiyitsa.
20 Iye anati, "Ndidzawabisira nkhope yanga,

ndi kuona kuti mathero awo adzakhala otani;
pakuti ndi m'bado wopotoka,
ana amene ndi osakhulupirika.
21 Anandichititsa kukhala wansanje pamene ankapembedza chimene si mulungu
ndi kundikwiyitsa chifukwa cha mafano awo achabechabe.
Ine ndidzawachititsa kuti achite nsanje ndi mtundu wina wopandapake;
ndidzawakwiyitsa ndi mtundu wina wachabechabe.
22 Pakuti mkwiyo wanga wayaka ngati moto,
umene umayaka mpaka ku dziko la anthu akufa.
Motowo udzanyeketsa dziko lapansi ndi zokolola zake
ndipo udzapsereza maziko a mapiri.

23 "Ndidzawawunjikira masautso
ndipo mivi yanga yonse idzathera pa iwo.
24 Ndidzawatumizira njala yoopsa,
malungo woopsa ndi nthenda zofa nazo;
ndidzawatumizira zirombo zakuthengo zowavuta,
ululu wa njoka ya m'phiri imene imakwawa pa fumbi.
25 M'misewu lupanga lidzawasandutsa kukhala wopanda ana;
mantha adzalamulira nyumba zawo.
Anyamata ndi atsikana adzafa,
ngakhalenso makanda ndi okalamba.
26 Ine ndinanena kuti ndidzawamwaza
ndi kuwafafaniza kuti anthu asawakumbukirenso,
27 koma sindinafune kuti adani anga adzandinyoze,
mwina adani anga sadzandimvetsetsa
ndipo adzanena kuti, 'Tagonjetsa anthuwa ndife;
Yehova sanachite zonsezi.' "

28 Iwo ndi mtundu wopanda maganizo,
iwo alibe nzeru n'pang'ono pomwe.
29 Ngati iwo akanakhala anzeru akanamvetsetsa izi
ndi kuzindikira kuti mathero awo adzakhala otani!
30 Kodi munthu mmodzi akanathamangitsa bwanji anthu 1,000
kapena anthu awiri kuthamangitsa anthu 10,000, kuti awagonjetse,
Thanthwe lawo likanapanda kuwagulitsa,
Yehova akanapanda kuwataya?
31 Pakuti thanthwe lawo silofanana ndi Thanthwe lathu,
ngakhale adani athu amavomereza zimenezi.
32 Mpesa wawo umachokera ku mpesa wa ku Sodomu
ndiponso ku minda ya ku Gomora.
Mphesa zawo zili ndi ululu wakupha
ndipo maphava ake ndi owawa.
33 Vinyo wawo ndi wa ululu wa njoka,
ululu woopsa wa mphiri.

34 "Kodi zimenezi sindinazisunge
ndi kuzitsekera m'katikati mwa chuma changa?
35 Kubwezera chilango n'kwanga; ndidzawalanga ndine.
Pa nthawi yake phazi lawo lidzaterera;
tsiku lawo la masautso layandikira

ndipo chiwonongeko chawo chikubwera pa iwo mofulumira."

36 Yehova adzaweruza anthu ake
ndipo adzachitira atumiki ake chifundo
pamene adzaona kuti mphamvu zawo zatha
ndipo kuti palibe amene watsala, kapolo kapena mfulu.
37 Iye adzanena kuti, "Nanga ili kuti milungu yawo,
thanthwe limene ankabisalamo,
38 milungu imene inkadya mafuta a nsembe zawo
ndi kumwa vinyo wa chopereka chawo cha chakumwa?"
Iwuzeni ibwere kuti idzakuthandizeni!
Ibwere kuti idzakutetezenitu!

39 "Onani tsopano kuti Ine ndine Iyeyo!
Palibe mulungu wina koma Ine ndekha.
Ine ndimapha ndiponso kupereka moyo,
ndavulaza ndipo ndidzachiritsa,
ndipo palibe angathe kupulumutsa munthu m'manja mwanga.
40 Ndikweza dzanja langa kumwamba ndi kulumbira kuti,
'Pali Ine wamoyo wamuyaya,
41 pamene ndidzanola lupanga langa lonyezimira
ndipo dzanja liligwira pakubweretsa chiweruzo,
ndidzabwezera chilango adani anga
ndi kulanga onse odana nane.
42 Mivi yanga idzakhuta magazi awo
pamene lupanga langa lidzawononga mnofu:
magazi a anthu ophedwa ndi ogwidwa ukapolo,
mitu ya atsogoleri a adani.' "

43 Kondwerani, inu mitundu yonse ya anthu pamodzi ndi anthu ake,
pakuti Iye adzabwezera chilango anthu amene anapha atumiki ake;
adzabwezera chilango adani ake
ndipo adzakhululukira dziko lake ndi la anthu ake.

44 Mose anabwera ndi Yoswa mwana wa Nuni ndipo anayankhula
mawu onsewa m'nyimbo anthu akumva. 45 Mose atatsiriza kunena
mawu onsewa pamtima kwa Aisraeli, 46 iye anawawuza kuti, "Muwasunge
bwino mu mtima mwanu, mawu onse amene lero lino ndikukuwuzani
kuti mudzawuze ana anu, kuti adzamvere mosamalitsa mawu onse a
malamulo amenewa. 47 Mawuwa sikuti ndi mawu achabe kwa inu.
Mawuwa ndi moyo wanu. Mukawamvera mudzakhala ndi moyo wautali
m'dziko limene mukukalitenga kukhala lanu mukawoloka Yorodani."

### *Mose Adzafera pa Phiri la Nebo*

48 Tsiku lomwelo Yehova anawuza Mose kuti, 49 "Pita ku mapiri a ku
Abarimu ukakwere pa Phiri la Nebo ku Mowabu, moyang'anana ndi
Yeriko, ndipo ukaone dziko la Kanaani, dziko limene ndikulipereka kwa
Aisraeli kukhala lawo. 50 Iwe udzafera pa phiri limenelo ndipo udzapita
kumene makolo ako anapita, monga m'bale wako Aaroni anafera pa
phiri la Hori ndipo anakakhala ndi anthu a mtundu wake. 51 Chifukwa
chake n'chakuti inu nonse awiri simunakhulupirike kwa Ine pamaso pa
Aisraeli pa madzi a Meriba ku Kadesi m'chipululu cha Zini chifukwa
simunandilemekeze kokwanira pakati pa Aisraeli. 52 Choncho udzalionera

kutali dziko limene ndikupereka kwa Aisraeli. Sudzalowa m'dziko limene ndi kulipereka kwa Aisraeli."

# 33

*Mose Adalitsa Mafuko a Aisraeli*

1 Awa ndi madalitso amene Mose, munthu wa Mulungu, anawapereka
kwa Aisraeli asanafe. 2 Iye anati:
"Yehova anabwera kuchokera ku Sinai
ndipo anatulukira kuchokera ku Seiri;
anawala kuchokera pa Phiri la Parani.
Iye anabwera ndi chiwunyinji cha angelo
kuchokera kummwera, moto woyaka uli m'dzanja mwake.
3 Ndithu ndinu amene mumakonda anthu anu;
opatulika ake onse ali m'manja mwake.
Onse amagwada pansi pa mapazi anu
kuchokera kwa inu amalandira malangizo,
4 malamulo amene Mose anatipatsa,
chuma chopambana cha mtundu wa Yakobo.
5 Iye anali mfumu ya Yesuruni
pamene atsogoleri a anthu anasonkhana,
pamodzi ndi mafuko a Israeli.

6 "Lolani Rubeni akhale ndi moyo ndipo asafe,
anthu ake asachepe pa chiwerengero."
7 Ndipo ponena za Yuda anati:
"Inu Yehova, imvani kulira kwa Yuda;
mubweretseni kwa anthu ake.
Ndi manja ake omwe adziteteze yekha.
Inu khalani thandizo lake polimbana ndi adani ake!"
8 Za fuko la Alevi anati:
"Tumimu wanu ndi Urimu ndi za
mtumiki wanu wokhulupirika.
Munamuyesa ku Masa;
munalimbana naye ku madzi a ku Meriba.
9 Iye ananena za abambo ake ndi amayi ake kuti,
'Sindilabadira za iwo.'
Sanasamale za abale ake
kapena ana ake,
koma anayang'anira mawu anu
ndipo anateteza pangano lanu.
10 Iye amaphunzitsa Yakobo malangizo anu
ndi malamulo anu kwa Israeli.
Amafukiza lubani pamaso panu
ndiponso amapereka nsembe zanu zonse zopsereza pa guwa lanu.
11 Inu Yehova, dalitsani luso lake lonse
ndipo mukondwere ndi ntchito za manja ake.
Menyani adani awo m'chiwuno
kanthani amene amuwukira kuti asadzukenso."
12 Za fuko la Benjamini anati:
"Wokondedwa wa Yehova akhale mwamtendere mwa Iye,
pakuti amamuteteza tsiku lonse,
ndipo amene Yehova amamukonda amawusa pa mapewa ake."

13 Za fuko la Yosefe anati:
“Yehova adalitse dziko lake
ndi mame ambiri ochokera kumwamba
ndiponso madzi ambiri ochokera pansi pa nthaka;
14 ndi zinthu zambiri zimene zimacha ndi dzuwa
ndiponso ndi zokolola zabwino kwambiri zimene zimacha ndi mwezi uliwonse;
15 ndi zipatso zabwino kwambiri zochokera m’mapiri amakedzanawa
ndiponso zokolola zochuluka zochokera ku zitunda zakalekale;
16 ndi mphatso zabwino kwambiri zochokera pa dziko lapansi ndi zonse zimene zili m’menemo
ndiponso kukoma mtima kwa Iye amene amakhala m’chitsamba choyaka moto.
Madalitso onsewa akhale pa mutu pa Yosefe,
wapaderadera pakati pa abale ake.
17 Ulemerero wake uli ngati ng’ombe yayimuna yoyamba kubadwa;
nyanga zake zili ngati za njati.
Ndi nyanga zakezo adzapirikitsa anthu a mitundu ina,
ngakhale iwo amene akukhala ku malekezero a dziko lapansi.
Nyanga zimenezi ndiye anthu miyandamiyanda a Efereimu;
nyanga zimenezi ndiye anthu 1,000 a Manase.”
18 Za fuko la Zebuloni anati:
“Kondwera Zebuloni, pamene ukutuluka,
ndipo iwe, Isakara, kondwera m’matenti ako.
19 Adzayitanira mitundu ya anthu kumapiri,
kumeneko adzaperekako nsembe zachilungamo;
kumeneko adzadyerera zinthu zochuluka zochokera ku nyanja,
chuma chobisika mu mchenga.”
20 Za fuko la Gadi anati:
“Wodala amene amakulitsa malire a Gadi!
Gadi amakhala kumeneko ngati mkango,
kukhadzula mkono kapena mutu.
21 Iye anadzisankhira dziko labwino kwambiri;
gawo la mtsogoleri anasungira iye.
Pamene atsogoleri a anthu anasonkhana,
anachita chifuniro cha Yehova molungama,
ndiponso malamulo onena za Israeli.”
22 Za fuko la Dani anati:
“Dani ndi mwana wamkango,
amene akutuluka ku Basani.”
23 Za fuko la Nafutali anati:
“Nafutali wadzaza ndi kukoma mtima kwa Yehova
ndipo ndi wodzaza ndi madalitso ake;
cholowa chake chidzakhala mbali ya kummwera kwa nyanja.”
24 Za fuko la Aseri anati:
“Mwana wodalitsika kwambiri ndi Aseri;
abale ake amukomere mtima,
ndipo asambe mapazi ake m’mafuta.
25 Zotsekera za zipata zako zidzakhala za chitsulo ndi za mkuwa,
ndi mphamvu zako zidzakhala ngati masiku a moyo wako.

26 “Palibe wina wofanana ndi Mulungu wa Yesuruni,
amene amakwera pa thambo kukuthandizani

ndiponso pa mitambo ya ulemerero wake.
27 Mulungu wamuyaya ndiye pothawirapo pathu,
ndipo pa dziko lapansi amakusungani ndi mphamvu zosatha.
Adzathamangitsa patsogolo panu mdani wanu,
adzanena kuti, 'Muwonongeni!'
28 Motero Israeli adzakhala yekha mwamtendere;
zidzukulu za Yakobo zili pa mtendere
m'dziko la tirigu ndi vinyo watsopano,
kumene thambo limagwetsa mame.
29 Iwe Israeli, ndiwe wodala!
Wofanana nanu ndani
anthu opulumutsidwa ndi Yehova?
Iye ndiye chishango ndi mthandizi wanu
ndi lupanga lanu la ulemerero.
Adani ako adzakugonjera,
ndipo iwe udzapondereza pansi malo awo achipembedzo."

# 34

*Mose Amwalira*

1 Ndipo Mose anakwera Phiri la Nebo kuchokera ku chigwa cha
Mowabu ndi kukafika pamwamba pa Phiri la Pisiga, kummawa kwa
Yeriko. Kumeneko Yehova anamuonetsa dziko lonse; kuchokera ku
Giliyadi mpaka ku Dani. 2 Dera lonse la Nafutali, dziko lonse la Efereimu
ndi Manase, dziko lonse la Yuda mpaka kukafika kumadzulo kwa nyanja,
3 Negevi ndi chigawo chonse kuchokera ku Chigwa cha Yeriko, Mzinda wa
mitengo ya migwalangwa, mpaka ku Zowari. 4 Kenaka Yehova anawuza
Mose kuti, "Limenelo ndi dziko limene ndinalonjeza mwa lumbiro kwa
Abrahamu, Isake ndi Yakobo pamene ndinanena kuti, 'Ndidzalipereka
kwa zidzukulu zanu.' Ndakulola kuti ulione, koma sudzawoloka kuti
ukalowemo."
5 Choncho Mose mtumiki wa Yehova anamwalira kumeneko ku Mowabu,
monga momwe ananenera Yehova. 6 Yehova anamuyika m'manda ku
Mowabu, m'chigwa choyang'anana ndi Beti-Peori, koma mpaka lero
palibe amene amadziwa pamene pali manda ake. 7 Mose anamwalira ali
ndi zaka 120, koma maso ake ankaonabe ndipo anali amphamvu. 8 Aisraeli
analira maliro a Mose m'chikhwawa cha Mowabu kwa masiku makumi
atatu mpaka nthawi ya kulira maliro ndi kukhuza inatha.
9 Tsono Yoswa, mwana wa Nuni anadzazidwa ndi mzimu wanzeru chifukwa n'kuti Mose atamusanjika manja. Choncho Aisraeli anamumvera
ndipo anachita zomwe Yehova analamula Mose.
10 Kuyambira nthawi imeneyi, mu Israeli simunakhalepo mneneri
wina aliyense wofanana ndi Mose, amene Yehova amayankhula naye
maso ndi maso. 11 Amene anachita zizindikiro zozizwitsa zonsezi ndi
zozizwitsa zimene Yehova anamutuma kuti achite mu Igupto, kwa Farao
ndi kwa nduna zake zonse ndiponso m'dziko lake lonse. 12 Ndithudi
palibe mneneri wina aliyense amene anachita zinthu zazikulu ndi zoopsa
zofanana ndi zomwe Mose anachita pamaso pa Aisraeli onse.

# Yoswa

*Yehova Asankha Yoswa Kukhala Mtsogoleri*

1 Atamwalira Mose mtumiki wa Mulungu, Yehova anati kwa Yoswa
mwana wa Nuni mthandizi wa Mose: 2 "Mose mtumiki wanga wamwalira.
Ndipo iwe ndi anthu onsewa, tsopano konzekani kuwoloka mtsinje wa
Yorodani kupita ku dziko limene ndiwapatse Aisraeli onse. 3 Paliponse
pamene phazi lanu liponde, ndikupatsani monga momwe ndinalonjezera
Mose. 4 Dziko lanu lidzayambira ku chipululu kummwera mpaka ku
mapiri a Lebanoni kumpoto, kuchokeranso ku mtsinje waukulu wa Yufu-
rate kummawa, mpaka dziko lonse la Ahiti, kukafika ku Nyanja Yayikulu
ya kumadzulo. 5 Palibe munthu amene adzatha kukugonjetsa masiku
onse a moyo wako. Monga Ine ndinakhalira ndi Mose, chomwechonso
ndidzakhala nawe. Sindidzakusiya kapena kukataya.

6 "Ukhale wamphamvu ndi wolimba mtima, chifukwa iwe udzatsogolera
anthu awa kukalandira dziko limene Ine ndinalonjeza makolo awo kuti
ndidzawapatsa. 7 Ukhale wamphamvu ndi wolimba mtima kwambiri.
Usamale ndithu kuti umvere malamulo onse amene mtumiki wanga
Mose anakupatsa. Usachoke pa malamulo anga ndipo kulikonse kumene
udzapite udzapambana. 8 Uziwerenga Buku la Malamuloli, uzilingalira
zolembedwa m'menemo usana ndi usiku, kuti uchite zonse zimene
zinalembedwamo. Ukamatero udzapeza bwino ndi kupambana. 9 Paja
ndinakulamula kuti ukhale wamphamvu ndi wolimba mtima. Choncho
usamachite mantha kapena kutaya mtima popeza Ine Yehova Mulungu
wako ndidzakhala nawe kulikonse kumene udzapite."

10 Tsono Yoswa analamula atsogoleri a Aisraeli nawawuza kuti, 11 "Pitani
ku misasa yonse ndipo muwuze anthu kuti, 'Konzekani, mangani katundu
wanu, popeza pakapita masiku atatu kuyambira lero mudzawoloka
Yorodani kupita kukatenga dziko limene Yehova Mulungu wanu akuku-
patsani.' "

12 Koma Yoswa anawuza fuko la Rubeni, fuko la Gadi ndi theka la
fuko la Manase kuti, 13 "Kumbukirani zimene Mose mtumiki wa Yehova
anakulamulani kuti, 'Yehova Mulungu wanu akukupatsani mpumulo, ndi
dziko ili kuti likhale lanu.' 14 Tsono akazi anu, ana anu ndi ziweto zanu
zitsale m'dziko lino limene Mose anakupatsani kummawa kwa Yorodani.
Koma ankhondo anu okha ndiwo awoloke atatenga zida zawo ndi kupita
patsogolo pa abale anu kukawathandiza. 15 Abale anuwo akadzalandira
dziko limene Yehova Mulungu wanu akuwapatsa monga inu mwachitira,
inu mudzabwerera kudzakhazikika m'dziko lanu limene Mose mtumiki
wa Yehova anakupatsani tsidya la kummawa kwa Yorodani."

16 Kenaka iwo anayankha Yoswa kuti, "Ife tidzachita chilichonse
chimene mwatilamula, ndipo kulikonse kumene mudzatitume tidzapita.
17 Monga momwe tinamvera Mose kwathunthu, chomwechonso tidza-
kumvera iwe. Yehova Mulungu wanu akhale nanu monga momwe
anachitira ndi Mose. 18 Aliyense wotsutsana ndi inu kapena wosamvera
zimene mutilamula adzaphedwa. Inu mukhale wamphamvu ndi wolimba
mtima!"

# 2

*Rahabe ndi Anthu Ozonda Dziko*

1 Tsono Yoswa mwana wa Nuni anatuma anthu awiri okazonda dziko
mwachinsinsi kuchokera ku Sitimu. Iye anawawuza kuti, “Pitani mukaone
dzikolo makamaka mzinda wa Yeriko.” Kotero iwo anapita ndipo
anakafika ku nyumba ya mkazi wadama dzina lake Rahabe, ndipo
anagona kumeneko.

2 Mfumu ya Yeriko inawuzidwa kuti, “Aisraeli ena afika mu mzinda
muno usiku uno kudzazonda dziko.” 3 Choncho Mfumu ya Yeriko
inatumiza uthenga kwa Rahabe kuti, “Atulutse anthu amene abwera ku
nyumba kwakowo chifukwa iwo abwera kuti adzazonde dzikoli.”

4 Koma pa nthawiyi n’kuti mkaziyo atatenga amuna awiriwo ndi
kuwabisa. Tsono anayankha kuti, “Inde, anthuwo anafikadi ku nyumba
kuno. Koma sindinadziwe kumene anachokera. 5 Iwo achoka kuno
ndi chisisira, chipata cha mzinda chili pafupi kutsekedwa. Ndiye
sindidziwa kumene alowera. Koma mukawalondola msanga muwapeza.”
6 Koma n’kuti atawakweza pa denga azondiwo ndi kuwabisa pansi pa
mapesi a thonje amene iye anawayika pa dengapo. 7 Nthumwi za
mfumu zija zitatuluka ndipo chipata chinatsekedwa. Nthumwizo zinapita
kukawafunafuna azondi aja mpaka ku dooko la Yorodani.

8 Azondiwo asanagone, Rahabe anakwera pa denga 9 ndipo anawawuza
kuti, “Ine ndikudziwa kuti Yehova wakupatsani dziko lino ndipo tili ndi
mantha. Anthu onse a m’dziko lino ali ndi mantha chifukwa cha inu.
10 Ife tinamva mmene Yehova anawumitsira madzi a Nyanja Yofiira inu
mukufika pamene munatuluka m’dziko la Igupto. Tamvanso zimene
munachita kwa Sihoni ndi Ogi, mafumu awiri a Aamori amene ali
kummawa kwa Yorodani. Inu munawawononga kotheratu. 11 Titamva
zimenezi, ife tinataya mtima ndipo aliyense wa ife ali ndi mantha
chifukwa cha inu. Tikudziwa kuti Yehova Mulungu wanu ndi Mulungu wa
kumwamba ndi dziko lapansi. 12 Choncho mulumbire pamaso pa Yehova
ndi kundipatsa chizindikiro choti mudzachitadi zimene mwalonjeza, kuti
monga inu ndakuchitirani chifundo, inunso mudzachitira chifundo a pa
banja la abambo anga. 13 Inu mulonjeze kuti simudzapha abambo anga
ndi amayi anga, abale anga ndi alongo anga ndi mabanja awo omwe.”

14 Anthuwo anamuyankha kuti, “Ife ndife okonzeka kufa chifukwa cha
inu. Ngati iwe sudzawulula zimene tachitazi, ndiye kuti ife tidzakukomera
mtima ndi kusunga pangano lathu ndi iwe, Yehova akadzatipatsa dziko
lino.”

15 Popeza nyumba ya Rahabe inali pa linga la mzindawo, azondi aja
anatulukira pa zenera. Rahabe anawatsitsa pansi ndi chingwe. 16 Iye
anawawuza kuti, “Pitani ku mapiri kuti okuthamangiraniwo asakupezeni.
Mukabisale kumeneko masiku atatu mpaka iwo atabwerera, ndipo kenaka
muzikapita kwanu.”

17 Anthuwo anati kwa iye, “Lonjezo limene watichititsa ifeli tidzal-
isungadi 18 tikadzalowa m’dzikoli, iwe udzamangirire kansalu kofiira pa
zenera limene unatitulutsira, ndi kusonkhanitsa abambo ako, amayi ako,
abale ako ndi banja lako lonse m’nyumba muno. 19 Ngati wina aliyense
adzatuluka m’nyumbamo kuti azikayendayenda mu msewu, magazi ake
adzakhala pamutu pake, ife sitidzapalamula kanthu. Koma wina aliyense
wokhala m’nyumba mwakomo akadzaphedwa, mlandu udzakhala wathu.

20 Komanso iwe ukangowulula zimene ife tikuchitazi ndiye kuti ife
sitidzasunga zimene talonjezazi.”
21 Rahabe anayankha kuti, “Zikhale monga mwaneneramo.” Kenaka iye
anawatulutsa ndipo iwowo anapita. Pambuyo pake Rahabe anamangirira
kansalu kofiira pa zenera paja.
22 Azondi aja anachoka napita ku mapiri ndipo anakhalako masiku
atatu. Apa n’kuti otumidwa ndi mfumu aja atawafunafuna ponseponse
n’kubwerera osawapeza. 23 Pambuyo pake azondi awiri aja anayamba
ulendo wobwerera kwawo. Anatsika ku mapiri kuja, nawoloka mtsinje
mpaka anakafika kwa Yoswa mwana wa Nuni. Ndipo anamuwuza
zonse zimene zinawachitikira. 24 Iwo anati kwa Yoswa, “Ndithu, Yehova
wapereka dziko lonse m’manja mwathu. Anthu onse kumeneko akuchita
nafe mantha.”

# 3

*Aisraeli Awoloka Yorodani*

1 Yoswa ndi Aisraeli onse anadzuka mmamawa nanyamuka ku Sitimu
kupita ku Yorodani. Iwo anagona kumeneko asanawoloke mtsinje wa
Yorodaniwo. 2 Patatha masiku atatu, atsogoleri anayendera misasa yonse,
3 kulangiza anthu kuti, “Mukaona ansembe a Chilevi atanyamula Bokosi
la Chipangano la Yehova Mulungu wanu, inu munyamuke pa malo ano
ndi kumalitsatira. 4 Potero mudzadziwa njira yoti mudzere, popeza
simunayendepo njira ino n’kale lomwe. Koma musaliyandikire. Pakati
pa inu ndi bokosilo pakhale mtunda pafupifupi kilomita imodzi.”
5 Yoswa anawuza anthu kuti, “Dzipatuleni tsono pakuti mawa Yehova
adzachita zodabwitsa pakati panu.”
6 Mmawa mwake Yoswa ananena kwa ansembe kuti, “Nyamulani Bokosi
la Chipangano muwoloke ndipo mukhale patsogolo pa anthu.” Motero iwo
analinyamula ndi kupita patsogolo pawo.
7 Ndipo Yehova anati kwa Yoswa, “Lero Ine ndidzayamba kukukweza
pamaso pa Aisraeli onse kuti adziwe kuti ndili nawe monga ndinalili ndi
Mose. 8 Ansembe amene akunyamula Bokosi la Chipangano uwalamule
kuti, ‘Mukafika ku mtsinje wa Yorodani mulowe mu mtsinjemo ndi kuyima
m’mphepete.’ ”
9 Yoswa anati kwa Aisraeli, “Bwerani pano mudzamve mawu a Yehova
Mulungu wanu. 10 Umu ndi mmene mudzadziwira kuti Mulungu
wamoyo ali pakati panu. Inu mukamadzapita patsogolo Iye adzathaman-
gitsa Akanaani, Ahiti, Ahivi, Aperezi, Agirigasi, Aamori ndi Ayebusi.
11 Pamenepo, Bokosi la Chipangano la Mbuye wa dziko lonse lapansi
lidzawoloka mu Yorodani patsogolo panu. 12 Musankhe amuna khumi ndi
awiri kuchokera ku fuko lililonse la Israeli. 13 Mapazi a ansembe onyamula
Bokosi la Yehova, Mbuye wa dziko lapansi, akadzangoponda mu Yorodani,
madzi ake onse ochokera ku mtunda adzaleka kuyenda ndipo adzayima
ngati chipupa.”
14 Tsono Aisraeli anachoka ku misasa yawo kukawoloka mtsinje wa
Yorodani. Ansembe onyamula Bokosi la Chipangano ndiwo anatsogolera
anthuwo. 15 Nyengo imeneyi inali yokolola ndipo mtsinje wa Yorodani
umakhala wodzaza. Komabe, ansembe onyamula Bokosi la Chipangano
anafika ku Yorodani, ndipo atangoponda m’madzimo, 16 madzi ochokera
ku mtunda anasiya kuyenda. Madzi a Yorodani ochokera ku mtunda
anawunjikana pamodzi ngati khoma lalitali pa mtunda wautali ndithu ndi

mzinda wa Adama chapafupi ndi mzinda wa Zaretani. Madzi othamangira
ku nyanja ya Araba, ngakhalenso amene amachokera kuti Nyanja ya
Mchere amathera pamenepo. Choncho anthu anawoloka tsidya lina
moyang'anana ndi Yeriko. 17 Ansembe onyamula Bokosi la Chipangano
la Yehova anali chiyimire powuma, pakati pa Yorodani pamene Aisraeli
amawoloka mpaka gulu lonse linamaliza kuwoloka powuma.

# 4

1 Anthu onse atatha kuwoloka Yorodani, Yehova anati kwa Yoswa,
2 "Sankha amuna khumi ndi awiri, mmodzi pa fuko lililonse. 3 Tsono
uwalamule kuti, 'Tengani miyala khumi ndi iwiri pakati penipeni pa
mtsinje wa Yorodani, pamalo pamene ansembe anayimirirapo. Miyalayo
muwoloke nayo ndi kudzayitula pamalo pamene mukagone usiku uno.' "

4 Choncho Yoswa anayitana amuna khumi ndi awiri amene
anawasankha aja kuchokera pakati pa Aisraeli, mmodzi pa fuko lililonse,
5 ndipo anawawuza kuti, "Lowani pakati pa mtsinje wa Yorodani,
patsogolo pa Bokosi la Yehova Mulungu wanu. Ndipo aliyense wa
inu atenge mwala pa phewa lake, monga mwa chiwerengero cha mafuko
a Aisraeli, 6 kuti ikhale chizindikiro kwa inu. M'tsogolo muno ana
anu akamadzakufunsani kuti, 'Kodi miyala iyi ikutanthauza chiyani?'
7 Muzidzawawuza kuti, 'Madzi a Yorodani analeka kuyenda pamene
Bokosi la Chipangano la Yehova linkawoloka mtsinjewo. Miyala iyi
idzakhala chikumbutso kwa anthu a Israeli kwa muyaya.' "

8 Aisraeli anachitadi monga Yoswa anawalamulira. Iwo ananyamula
miyala khumi ndi iwiri kuchokera pakati pa Yorodani, fuko lililonse la
Israeli mwala wake, monga Yehova analamulira Yoswa. Miyalayo anapita
nayo ku misasa yawo nakayikhazika kumeneko. 9 Yoswa anayimika
miyala khumi ndi iwiri imene inali pakati pa Yorodani pamalo pamene
ansembe onyamula Bokosi la Chipangano anayimapo. Ndipo miyalayo ili
pamalo pomwepo mpaka lero lino.

10 Ansembe onyamula Bokosi lija anayimirirabe pakati pa Yorodani
mpaka zonse zimene Yehova analamulira Yoswa kuti awuze anthu zinatha.
Zimenezi zinali monga momwe Mose anamufotokozera Yoswa. Tsono
anthu anawoloka mtsinjewo mofulumira. 11 Anthu atatha kuwoloka,
ansembe anatsogolera anthuwo atanyamula Bokosi la Yehova. 12 Anthu
a fuko la Rubeni, Gadi ndi theka la fuko la Manase anawoloka patsogolo
pa Aisraeli ali ndi zida, monga momwe Mose anawalamulira. 13 Asilikali
pafupifupi 40,000 anawoloka napita kukayima m'chigwa cha Yeriko
kukonzekera nkhondo.

14 Zimene Yehova anachita tsiku limeneli zinapatsa anthu mtima
wolemekeza Yoswa. Ndipo anamulemekeza masiku onse a moyo wake,
monga momwe analemekezera Mose.

15 Kenaka Yehova anati kwa Yoswa, 16 "Lamula ansembe onyamula
Bokosi la Chipanganowo kuti atuluke mu Yorodani."

17 Choncho Yoswa anawalamuladi ansembe aja kuti atuluke mu Yoro-
dani muja.

18 Ansembe onyamula Bokosi la Chipangano la Yehova aja atangotuluka
mu mtsinje muja n'kuponda powuma, madzi a mu Yorodani anayambanso
kuyenda ngati poyamba mpaka kumasefukira.

19 Aisraeli anawoloka Yorodani tsiku lakhumi la mwezi woyamba
ndipo anakamanga misasa yawo ku Giligala mbali ya kummawa kwa

Yeriko. [20] Ku Giligala, Yoswa anayimikako miyala khumi ndi iwiri imene
anayitenga mu Yorodani ija. [21] Ndipo iye anati kwa Aisraeli, "M'tsogolo
muno pamene adzukulu anu adzafunsa makolo awo kuti, 'Kodi miyala
iyi ikutanthauza chiyani?' [22] Muzidzawawuza kuti, 'Aisraeli anawoloka
Yorodani pansi pali powuma.' [23] Pakuti Yehova Mulungu wanu ndiye
anawumitsa Yorodani pamaso panu mpaka inu mutawoloka. Yehova
Mulungu wanu anaphwetsa madzi a Yorodani monga mmene anachitira
ndi Nyanja Yofiira mpaka ife tinawoloka powuma. [24] Iye anachita zimenezi
kuti anthu onse pa dziko lapansi adziwe kuti dzanja la Yehova ndi
lamphamvu, ndi kuti inu muziopa Yehova Mulungu wanu masiku onse."

# 5

*Mwambo wa Mdulidwe pa Giligala*

[1] Mafumu onse a Aamori, a kummawa kwa Yorodani ndi mafumu onse a
Akanaani a m'mbali mwa Nyanja anamva momwe Yehova anawumitsira
Yorodani pamene Aisraeli ankawoloka. Choncho anachita mantha ndi
kutayiratu mtima chifukwa cha Aisraeliwo.

[2] Tsono Yehova anati kwa Yoswa, "Panga mipeni ya miyala ndipo
uchitenso mwambo wa mdulidwe pa Aisraeli." [3] Choncho Yoswa anapanga
mipeni ya miyala ndi kuchita mdulidwe Aisraeli ku Gibeyati Haaraloti.

[4] Chifukwa chimene Yoswa anachitira izi ndi ichi: Onse amene
anatuluka m'dziko la Igupto, amuna onse amene anali oyenera kumenya
nkhondo anatha kufa m'chipululu atatuluka m'dziko la Igupto. [5] Anthu
onse amene anatuluka m'dziko la Igupto anali atachita mwambo wa
mdulidwe, koma onse amene anabadwira m'chipululu, pa ulendo wo-
choka ku Igupto, sanachite. [6] Aisraeli anakhala akuyenda m'chipululu
kwa zaka makumi anayi mpaka amuna onse amene potuluka m'dziko la
Igupto anali a msinkhu woyenera kupita ku nkhondo anamwalira. Iwo
anafa chifukwa sanamvere mawu a Yehova. Yehova anawalumbirira kuti
sadzalowa konse m'dziko loyenda mkaka ndi uchi limene analonjeza kwa
makolo awo kuti adzatipatsa. [7] Koma ana awo amene analowa m'malo
mwawo ndiwo amene Yoswa anawachita mdulidwe popeza sanachite
pamene anali pa ulendo wawo m'chipululu muja. [8] Atamaliza kuchita
mdulidwe uja, anthu onse anakakhala ku misasa yawo kudikira kuti
zilonda zipole.

[9] Kenaka Yehova anati kwa Yoswa, "Kuyambira tsopano anthu a ku
Igupto sadzakunyozaninso." N'chifukwa chake malowa anatchedwa
Giligala mpaka lero.

[10] Akupumulabe ku Giligala kuja m'chigwa cha Yeriko, Aisraeli anachita
chikondwerero cha Paska madzulo pa tsiku la 14 la mwezi woyamba
womwewo. [11] Mmawa mwake ndi pamene anayamba kudya zakudya za
m'dziko la Kanaani. Anaphika buledi wopanda yisiti ndi kukazinga tirigu
tsiku lomwelo. [12] Atangodya chakudya cha m'dzikomo, mana anasiya
kugwa, ndipo sanapezekenso. Kuyambira nthawi imeneyo Aisraeli
anayamba kudya chakudya cha m'dziko la Kanaani.

*Kugwa kwa Makoma a Yeriko*

[13] Tsiku lina pamene Yoswa anali pafupi ndi Yeriko, anakweza maso ake
ndipo mwadzidzidzi anaona munthu atayima patsogolo pake ndi lupanga
losolola m'dzanja lake. Yoswa anapita pamene panali munthuyo ndipo
anamufunsa kuti, "Kodi uli mbali yathu kapena ya adani athu?"

14 Iye anayankha kuti “Sindili mbali iliyonse. Ndabwera monga mkulu
wa asilikali a Yehova.” Pomwepo Yoswa anadzigwetsa chafufumimba
kupereka ulemu, ndipo anamufunsa, “Kodi mbuye wanga muli ndi
uthenga wotani kwa mtumiki wanu?”

15 Mkulu wa asilikali a Yehova uja anayankha kuti, “Vula nsapato zako,
pakuti wayima pa malo wopatulika.” Ndipo Yoswa anachitadi zimene
anawuzidwazo.

# 6

1 Tsono mzinda wa Yeriko unali utatsekedwa kuti Aisraeli asalowe.
Palibe amene amatuluka kapena kulowa.

2 Kenaka Yehova anati kwa Yoswa, “Taona ndapereka Yeriko, pamodzi
ndi mfumu yake ndi ankhondo ake m’manja mwako. 3 Tsono iwe
pamodzi ndi ankhondo ako onse muzizungulira mzindawu masiku asanu
ndi limodzi, kamodzi pa tsiku. 4 Ansembe asanu ndi awiri, atanyamula
malipenga a nyanga za nkhosa zazimuna, akhale patsogolo pa Bokosi la
Chipangano. Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri mudzazungulire mzindawu
kasanu ndi kawiri ansembe akuliza malipenga. 5 Ansembe adzalize
malipenga kosalekeza. Tsono anthu onse akadzamva kuliza kumeneku
adzafuwule kwambiri, ndipo makoma a mzindawo adzagwa. Zikadzatero
ankhondo adzalowe mu mzindawo.”

6 Ndipo Yoswa mwana wa Nuni anayitana ansembe ndipo anawawuza
kuti, “Nyamulani Bokosi la Chipangano cha Yehova ndipo ansembe asanu
ndi awiri anyamule malipenga. Iwowa akhale patsogolo pake.” 7 Ndipo
analamulira anthu kuti, “Yambani kuyenda! Yendani mozungulira mzinda
ndipo ankhondo akhale patsogolo pa Bokosi la Yehova.”

8 Mofanana ndi mmene Yoswa anayankhulira kwa anthu aja, ansembe
asanu ndi awiri anapita patsogolo pa Bokosi la Chipangano la Yehova
akuliza malipenga a nyanga za nkhosa zija, ndipo Bokosi la Chipangano
cha Yehova limabwera pambuyo pawo. 9 Ankhondo amayenda patsogolo
pa ansembe amene amayimba malipenga, ndiponso gulu lina pambuyo
pa Bokosilo. Nthawi yonseyi n’kuti malipenga akulira. 10 Koma Yoswa
n’kuti atalamulira anthu kuti, “Musafuwule, musakweze mawu anu
kapena kuyankhula mpaka tsiku limene ndidzakuwuzani kuti mufuwule.
Pamenepo mudzafuwule!” 11 Ansembe onyamula Bokosi la Chipangano la
Yehova anazungulira mzindawo kamodzi. Kenaka anthu anabwerera ku
msasa wawo kukagona.

12 Yoswa anadzuka mmawa tsiku linalo ndipo ansembe ananyamula
Bokosi la Yehova. 13 Ansembe asanu ndi awiri onyamula malipenga asanu
ndi awiri anakhala patsogolo pa Bokosi la Yehova akuyimba malipenga.
Ankhondo anali patsogolo pawo ndipo gulu lina linatsatira Bokosi la
Yehova. Apa n’kuti malipenga akulira. 14 Tsiku lachiwiri anazunguliranso
mzinda kamodzi ndi kubwerera ku misasa. Iwo anachita izi kwa masiku
asanu ndi limodzi.

15 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, anadzuka m’bandakucha ndipo
anazungulira mzindawo kasanu ndi kawiri. Ndi pa tsiku lokhali limene
anazungulira mzindawu kasanu ndi kawiri. 16 Pomwe amazungulira
kachisanu ndi chiwiri, ansembe akuliza malipenga mokweza, Yoswa
analamulira anthu kuti “Fuwulani pakuti Yehova wakupatsani mzindawu!
17 Mzindawu ndi zonse zimene zili m’menemo muziwononge. Rahabe
yekha, mayi wadama, ndi aliyense amene ali pamodzi naye m’nyumba

mwake asaphedwe, chifukwa anabisa anthu odzazonda, amene ife tinawa-
tuma 18 Koma musatenge kanthu kalikonse koyenera kuwonongedwa.
Mukadzangotenga kanthu kalikonse koyenera kuwonongedwa, mudza-
puta mavuto, misasa ya Israeli idzawonongedwa. 19 Zonse za siliva ndi
golide, ziwiya zamkuwa ndi zachitsulo, ndi zake za Yehova ndipo ziyenera
kukasungidwa mosungiramo chuma chake."

20 Ansembe analiza malipenga. Anthu atamva kulira kwa malipenga,
anafuwula kwambiri ndipo makoma a Yeriko anagwa. Choncho ankhondo
anabwera ku mzinda uja nawulanda. 21 Iwo analowa mu mzindawo
nawononga ndi lupanga chilichonse chamoyo kuyambira amuna, akazi,
ana ndi akulu, ng'ombe, nkhosa ndi abulu.

22 Yoswa anawuza anthu awiri amene anakazonda dziko aja kuti, "Pitani
ku nyumba ya mkazi wadama uja ndipo mukamutulutse iye pamodzi ndi
onse amene ali naye ndipo mukabwere nawo kuno, munamulumbirira."
23 Choncho iwo anapita nakatenga Rahabe, abambo ake ndi amayi ake,
abale ake ndi onse amene anali naye. Iwo anatulutsa banja lake lonse
ndipo analiyika kuseri kwa msasa wa Aisraeli.

24 Kenaka iwo anawotcha mzinda wonse ndi chilichonse chimene
chinali m'menemo, kupatulapo zasiliva ndi zagolide pamodzi ndi ziwiya
zamkuwa ndi zachitsulo zimene anakaziyika m'nyumba yosungiramo
chuma cha Yehova. 25 Koma Yoswa sanaphe Rahabe, mkazi wadamayo
pamodzi ndi banja lake ndi onse amene anali naye, chifukwa anabisa
anthu amene iye anawatuma kukazonda Yeriko. Zidzukulu zake za
Rahabeyo zikukhala pakati pa Aisraeli mpaka lero.

26 Pa nthawi imeneyo Yoswa anapereka chenjezo motemberera kuti,
"Akhale wotembereredwa pamaso pa Yehova munthu amene adzaman-
genso mzinda uwu wa Yeriko:

"Aliyense amene adzayike maziko ake,
mwana wake wamwamuna wachisamba adzafa,
aliyense womanga zipata zake
mwana wake wamng'ono adzafa."

27 Motero Yehova anali ndi Yoswa, ndipo mbiri yake inafalikira dziko
lonse.

# 7

*Tchimo la Akani*

1 Koma Aisraeli anachita zachinyengo ndi lamulo lija loti asatenge
kalikonse koyenera kuwonongedwa. Akani mwana wa Karimi, mwana wa
Zabidi, mwana wa Zera, wa fuko la Yuda anatengako zinthu zina. Choncho
Yehova anakwiyira Israeli kwambiri.

2 Tsono Yoswa anatuma anthu kuchokera ku Yeriko kukazonda ku
mzinda wa Ai umene uli pafupi ndi mzinda wa Beti-Aveni kummawa kwa
Beteli, ndipo anawawuza kuti, "Pitani mukazonde chigawochi." Anthuwo
anapitadi kukazonda Ai.

3 Atabwera kwa Yoswa, anamuwuza kuti, "Sikofunika kuti apite anthu
onse kukathira nkhondo mzinda wa Ai. Mutumizeko anthu 2,000 kapena
3,000 kuti akatenge mzindawo. Musawatume anthu onse kumeneko
popeza kuli anthu ochepa." 4 Choncho kunapita anthu 3,000. Koma iwo
anathamangitsidwa ndi anthu a ku Ai. 5 Anthu a ku Ai anathamangitsa
Aisraeli kuchokera pa chipata cha mzindawo mpaka ku ngwenya ndipo
anapha anthu 36. Iwowa anawapha pamene ankatsika phiri. Choncho
mitima ya anthu inasweka ndipo analibenso mphamvu.

6 Tsono Yoswa anang'amba zovala zake nagwada n'kuweramitsa mutu
wake pansi patsogolo pa Bokosi la Yehova. Akuluakulu a Israeli nawonso
anadzigwetsa pansi ndipo anakhala pomwepo mpaka madzulo atadziwaza
fumbi kumutu kwawo. 7 Ndipo Yoswa anati, "Kalanga ine, Ambuye
Wamphamvuzonse chifukwa chiyani munatiwolotsa Yorodani? Kodi
mumalinga zotipereka m'manja mwa Aamori kuti atiwononge chotere?
Kukanakhala kwabwino ife tikanakhala tsidya linalo la Yorodani! 8 Tsono
Ambuye, ine ndinene chiyani, pakuti tsopano Israeli anathamangitsidwa
ndi adani ake? 9 Akanaani ndi anthu ena a dziko lino adzamva zimenezi
ndipo adzatizinga ndi kutiwonongeratu. Nanga inu mudzatani ndi dzina
lanu lamphamvulo?"

10 Koma Yehova anati kwa Yoswa, "Imirira! Chifukwa chiyani wag-
wada pansi chotere? 11 Aisraeli achimwa. Iwo aphwanya pangano
limene ndinawalamula kuti asunge. Anatengako zinthu zina zofunika
kuwonongedwa. Choncho anabako, ananena bodza ndi kuyika zinthu
zakubazo pamodzi ndi katundu wawo. 12 N'chifukwa chake Aisraeli
sangathe kulimbana ndi adani awo. Iwo anathawa pamaso pa adani
awo chifukwa ndiwo oyenera kuwonongedwa. Ine sindikhalanso ndi inu
pokhapokha mutawononga chilichonse choyenera kuwonongedwa pakati
panu.

13 "Nyamuka, ukawawuze anthu kuti, 'Mudzipatule nokha kukonzekera
kuonana nane mawa; pakuti Yehova Mulungu wa Israeli akuti choyenera
kuwonongedwa chija chili pakati panu, inu Aisraeli. Simungathe kulim-
bana ndi adani anu mpaka mutachichotsa.'

14 "Mawa mmamawa adzabwere pamaso pa Yehova fuko limodzil-
imodzi. Fuko limene Yehova adzaliloze lidzabwere patsogolo mbumba
imodziimodzi. Tsono mbumba imene Yehova adzayiloze idzabwere pat-
sogolo banja limodzilimodzi. Banja limene Yehova adzaliloze lidzabwere
patsogolo munthu mmodzimmodzi. 15 Iye amene adzagwidwe ndi zinthu
zoyenera kuwonongedwazo adzawotchedwa ndi moto, pamodzi ndi banja
lake lonse ndi zinthu zake zonse. Iyeyutu wachita chinthu chonyansa
pakati pa Aisraeli ndi kuphwanya pangano limene anthu anga anachita
ndi Ine!"

16 Mmawa mwake Yoswa anabweretsa Israeli fuko limodzilimodzi ndipo
fuko la Yuda linalozedwa. 17 Anabweretsa poyera mbumba zonse za fuko
la Yuda, ndipo mbumba ya Zera inagwidwa. Kenaka anatulutsa poyera
mabanja onse a mbumba ya Zera ndipo banja la Zabidi linagwidwa.
18 Potsiriza anatulutsa anthu onse a banja la Zabidi ndipo Akani anag-
widwa. Iyeyu anali mwana wa Karimi, mwana wa Zabidi, mwana wa
Zera wa fuko la Yuda.

19 Ndipo Yoswa anati kwa Akani, "Mwana wanga pereka ulemerero
kwa Yehova Mulungu wa Israeli ndipo umuyamike Iye. Ndiwuze zimene
wachita, ndipo usandibisire."

20 Akani anayankha kuti, "Zoona! Ine ndachimwira Yehova Mulungu wa
Israeli. Chimene ndachita ine ndi ichi: 21 Ndinaona mwa zinthu zolanda
ku nkhondo zija, mkanjo wokongola wa ku Babuloni, makilogalamu
awiri a siliva ndiponso golide wolemera theka la kilogalamu. Zimenezi
ndinazikhumba ndipo ndinazitenga. Ndazibisa m'kati mwa tenti yanga,
ndipo siliva ali pansi pake."

22 Motero Yoswa anatuma anthu, ndipo anathamanga kupita ku tenti.
Anthuwo anakapeza kuti zinthuzo zinabisidwadi m'tenti yake, ndipo siliva

analidi pansi pake. [23] Iwo anazichotsa zinthuzo mu tenti yake nabwera
nazo kwa Yoswa ndi kwa Aisraeli onse ndipo anaziyika pamaso pa Yehova.
[24] Kenaka Yoswa pamodzi ndi Aisraeli onse anatenga Akani mwana
wa Zera pamodzi ndi siliva, mkanjo, golide zimene anapezeka nazo zija.
Anatenganso ana ake aamuna ndi aakazi, ng'ombe zake, abulu ndi nkhosa,
tenti yake ndi zonse anali nazo, kupita nazo ku chigwa cha Akori. [25] Yoswa
anati "Chifukwa chiyani wabweretsa mavuto awa pa ife? Yehova ndiye
abweretse mavuto pa iwe lero."

Kenaka Aisraeli onse anaponya miyala Akani, namupha. Anaponyanso
miyala banja lake lonse, n'kulipha. Pambuyo pake anatentha Akani uja,
banja lake ndi zonse zimene anali nazo. [26] Anawunjika mulu waukulu wa
miyala pa Akani, imene ilipobe mpaka lero. N'chifukwa chake malowa
amatchedwa chigwa cha Akori mpaka lero. Ndipo Yehova anachotsa
mkwiyo wake.

# 8

*Kuwononongedwa kwa Mzinda wa Ai*

[1] Kenaka Yehova anati kwa Yoswa, "Usachite mantha kapena kutaya
mtima. Tenga gulu lonse la nkhondo, ndipo upite ku Ai. Taona, ndapereka
mfumu ya Ai pamodzi ndi anthu ake, mzinda wake ndi dziko lake lonse
m'manja mwako. [2] Mzinda wa Ai ndi mfumu yake muchite monga
munachita ndi mzinda wa Yeriko ndi mfumu yake, koma katundu wa
mumzindamo ndi zoweta mukazitenge ndi kuzisunga kuti zikhale zanu.
Mukalalire mzinda wa Ai ndi kuwuthira nkhondo kuchokera kumbuyo."

[3] Kotero Yoswa ndi gulu lonse la nkhondo anakonzeka kupita ku Ai.
Iye anasankha amuna 30,000 odziwa kumenya nkhondo bwino ndipo
anawatumiza usiku [4] nawapatsa malamulo awa kuti, "Mvetsani bwino;
mukabisale kuseri kwa mzindawo. Musakapite patali ndi mzindawo,
koma nonsenu mukakhale okonzekera nkhondo. [5] Ine ndi gulu langa
lonse tikayamba kuwuputa mzindawu, ndipo akadzangotuluka kudza-
limbana nafe, ife tidzawathawa monga tinachitira poyamba. [6] Iwo
adzatithamangitsa mpaka titawakokera kutali ndi mzindawo, pakuti iwo
adzati, 'Akutithawa monga anachitira poyamba.' Pamene ife tizidzathawa,
[7] inu mudzatuluke pamene mwabisalapo ndi kulanda mzindawo. Yehova
Mulungu wanu adzakupatsani mzindawo. [8] Mukakawulanda mzindawo
mudzawuyatse moto. Mukachite monga mwa mawu a Yehova. Amenewa
ndiwo malamulo amene ndakupatsani."

[9] Yoswa atawatumiza, anapita ku malo wokabisalakowo ndipo
anadikirira kumeneko. Malowa anali pakati pa Beteli ndi Ai, kumadzulo
kwa Ai. Koma Yoswa anagona usiku umenewu pakati pa gulu lake
lankhondo.

[10] Mmawa mwake, Yoswa anadzuka nayitana asilikali ake. Tsono iye
pamodzi ndi akuluakulu a Aisraeli anatsogola kupita ku Ai. [11] Gulu
lonse la nkhondo limene linali ndi iye linatsogolako ndi kukamanga
zithando pafupi ndi mzindawo chakumpoto mopenyana nawo. Pakati
pa iwo ndi mzindawo panali chigwa. [12] Yoswa anali atatenga asilikali
5,000 ndi kuwabisa pakati pa Ai ndi Beteli, kumadzulo kwa mzindawo.
[13] Anakhazika anthuwo mokonzekera nkhondo. Gulu lalikulu la nkhondo
linakamanga zithando zawo kumpoto kwa mzinda, ndipo gulu lina
linakamanga zithando zawo kumadzulo kwa mzindawo. Usiku umenewo
Yoswa anakagona ku chigwa.

14 Mfumu ya Ai itaona ankhondo a Yoswa, inachita zinthu mofulumira.
Inadzuka mmamawa ndipo inapita pamodzi ndi anthu ake ku malo
otsika oyang'anana ndi Araba kuti akachite nkhondo ndi Aisraeli. Koma
iyo sinadziwe kuti ayithira nkhondo kudzera kumbuyo kwa mzindawo.
15 Yoswa ndi Aisraeli onse anachita ngati agonja ndi kumathawira ku
chipululu. 16 Anthu onse a ku Ai anawuzidwa kuti awapirikitse. Ndipo
iwo anapirikitsadi Yoswa uja, ndi kupita kutali ndi mzinda wawo.
17 Palibe munthu wamwamuna wa mzinda wa Ai kapena wa Beteli amene
sanatuluke kukapirikitsa Aisraeli. Iwo anasiya mzinda wosatseka ndi
kumapirikitsa Aisraeli.

18 Ndipo Yehova anati kwa Yoswa, "Loza mkondo uli m'dzanja lako
ku Ai pakuti ine ndipereka m'dzanja lanu mzindawo." Kotero Yoswa
analoza mkondowo ku Ai. 19 Atangotambalitsa dzanja lake, anthu
amene anabisala aja ananyamuka msangamsanga pamalo pawo ndi
kuthamangira kutsogolo. Iwo analowa mu mzindamo ndi kuwulanda
ndipo anawutentha mofulumira.

20 Anthu a ku Ai aja atangochewukira m'mbuyo anaona utsi uli tolotolo.
Koma mpata woti athawireko panalibe pakuti Aisraeli amene amathawira
ku chipululu anabwerera nayamba kuwathamangitsa. 21 Yoswa ndi
Aisraeli onse ataona kuti obisalira aja alanda mzinda ndipo kuti utsi
unali tolotolo, iwo anatembenuka ndi kuyamba kupha anthu a ku Ai.
22 Nawonso Aisraeli amene anali mu mzindamo anatuluka kudzalimbana
ndi anthu a ku Ai. Choncho iwo anazingidwa mbali zonse ndi Aisraeli
ndipo onse anaphedwa. Palibe amene anatsala wamoyo kapena wothawa
23 kupatula mfumu ya ku Ai yokha imene anayigwira nabwera nayo kwa
Yoswa.

24 Aisraeli aja atatha kupha anthu onse a ku Ai amene anali m'thengo
ndi m'chipululu kumene anawapirikitsira, onse anabwerera ku Ai ndi
kupha onse amene anali mu mzindamo. 25 Chiwerengero cha anthu onse
a ku Ai, amuna ndi akazi, amene anaphedwa pa tsiku limeneli chinali
12,000. 26 Yoswa sanatsitse dzanja lake limene ananyamula mkondo
mpaka ataona kuti onse amene amakhala mu mzinda wa Ai aphedwa.
27 Tsono Aisraeli anatenga zoweta ndi katundu yense wa anthu ophedwa
aja, monga momwe Yehova analamulira Yoswa.

28 Pambuyo pake Yoswa anawutentha mzinda wa Ai ndi kuwusiya
bwinja monga ulili leromu. 29 Iye anapachika pa mtengo mfumu ya
Ai ndipo anayisiya mpaka madzulo. Pomwe dzuwa linalowa Yoswa
analamula kuti akachotse mtembowo ndi kukawutaya ku chipata cha
mzindawo. Pamwamba pa mtembowo anawunjikapo mulu waukulu wa
miyala. Muluwo ulipobe mpaka lero lino.

### *Kuchitanso Pangano pa Phiri la Ebala*

30 Ndipo Yoswa anamanga guwa lansembe la Yehova Mulungu wa Israeli
pa phiri la Ebala. 31 Analimanga motsata zimene Mose mtumiki wa Yehova
analamulira Aisraeli, ndiponso potsata zomwe zinalembedwa m'buku la
malamulo a Mose kuti guwa lansembe likhale la miyala yosasemedwa
ndi chitsulo. Pa guwalo anapereka kwa Yehova nsembe yopsereza ndi
nsembe yachiyanjano. 32 Kenaka anthu onse akupenya, Yoswa analemba
pa miyala chitsanzo cha malamulo amene Mose analemba. 33 Aisraeli
onse, akuluakulu awo, atsogoleri awo ndi oweruza awo, alendo pamodzi
ndi mbadwa, anayimirira mbali zonse ziwiri za Bokosi la Chipangano la
Yehova, ena uku ena uku moyang'anana ndi ansembe a Chilevi. Theka la

anthu linayima patsogolo pa phiri la Gerizimu ndipo theka lina patsogolo pa phiri la Ebala, monga momwe Mose mtumiki wa Yehova anawalamulira m'mbuyomo pamene anawapatsa malangizo podalitsa Aisraeli.

34 Pambuyo pake Yoswa anawerenga mawu onse a malamulo, madalitso
ndi matemberero monga momwe zinalembedwera m'buku la malamulo a
Mose. 35 Yoswa anawerenga mawu onse amene Mose analamula, gulu
lonse la Israeli limene linasonkhana likumva. Amayi, ana ndi alendo
omwe okhala pakati pawo anali pomwepo.

# 9

*Chinyengo cha Agibiyoni*

1 Mafumu onse okhala kumadzulo kwa Yorodani atamva zimenezi
pamodzi ndi mafumu okhala ku mayiko a ku mapiri, mu zigwa, m'mbali
mwa Nyanja yayikulu mpaka ku Lebanoni (mafumu a Ahiti, Aamori,
Akanaani, Aperezi, Ahivi, ndi Ayebusi), 2 anapangana kuti achite nkhondo
ndi Yoswa ndi Israeli.
3 Koma Ahivi ena a ku Gibiyoni atamva zomwe Yoswa anachitira
mizinda ya Yeriko ndi Ai, 4 anaganiza zochita zachinyengo. Anapita nasen-
zetsa abulu awo chakudya m'matumba akalekale ndiponso matumba
a vinyo achikopa ong'ambikang'ambika. 5 Anthuwa anavala nsapato
zakutha ndi zazigamba ndiponso anavala sanza. Buledi wawo yense anali
wowuma ndi wowola. 6 Ndipo anapita kwa Yoswa ku msasa ku Giligala
ndikumuwuza kuti, pamodzi ndi Aisraeli onse, "Ife tachokera ku dziko
lakutali, ndipo tikufuna kuti muchite mgwirizano ndi ife."
7 Koma Aisraeli anayankha Ahiviwo kuti, "Mwinatu inu mukukhala
pafupi ndi ife. Tsono ife tingachite bwanji mgwirizano ndi inu?"
8 Iwo anati kwa Yoswa, "Ife ndife akapolo anu."

Tsono Yoswa anawafunsa kuti, "Inu ndinu yani ndipo mukuchokera kuti?"

9 Iwo anayankha kuti, "Akapolo anufe tachokera ku dziko lakutali
chifukwa tamva za Yehova Mulungu wanu. Tamva mbiri yonse ya zimene
Iye anachita ku Igupto, 10 ndi zonse zimene anachita kwa mafumu awiri
a Aamori kummawa kwa Yorodani, mfumu Sihoni ya Hesiboni ndi Ogi
mfumu ya Basani amene amalamulira ku Asiteroti. 11 Tsono akuluakulu
athu ndi onse amene akukhala m'dziko lathu anati kwa ife. Tengani
chakudya cha pa ulendo wanu. Pitani mukakumane nawo ndipo mukati
kwa iwo, 'Ife ndife akapolo anu, ndipo tikufuna kuti mugwirizane nafe
za mtendere.' " 12 Buledi wathuyu anali wotentha pamene timanyamuka
ku mudzi kubwera kwa inu. Koma tsopano taonani ali gwaa ndiponso
wawola. 13 Zikopa zimene tinathiramo vinyozi zinali zatsopano, koma
taonani zathetheka. Zovala zathu ndi nsapato zathu zatha chifukwa cha
kutalika kwa ulendo.
14 Aisraeli anatengako chakudya chawo koma sanafunse kwa Yehova.
15 Choncho Yoswa anapangana nawo za mtendere kuti sadzawapha, ndipo
atsogoleri a gulu anavomereza pochita lumbiro.
16 Patatha masiku atatu atachita mgwirizano wa mtendere ndi Agibiyoni,
Aisraeli anamva kuti anali anansi awo, anthu amene amakhala nawo
pafupi. 17 Tsono Aisraeli ananyamuka ulendo ndipo tsiku lachitatu anafika
ku mizinda ya Gibiyoni, Kefira, Beeroti ndi Kiriati-Yearimu. 18 Koma

Aisraeli sanawaphe anthuwo chifukwa atsogoleri awo anali atalonjeza m'dzina la Yehova Mulungu wa Israeli za Agibiyoniwo.

Koma anthu onse anatsutsana ndi atsogoleriwo. [19] Koma atsogoleriwo
anayankha kuti, "Ife tinawalonjeza m'dzina la Yehova, Mulungu wa
Israeli, ndipo tsopano sitingawaphe. [20] Chimene tidzachita nawo ndi ichi: Tidzawasiya akhale ndi moyo kuti mkwiyo wa Yehova usatigwere
chifukwa chophwanya lonjezo limene tinawalonjeza." [21] Anapitiriza kunena kuti "Asiyeni akhale ndi moyo, komabe akhale otidulira mitengo ndi kutitungira madzi ogwiritsa ntchito pa chipembedzo." Lonjezo la atsogoleriwo linasungidwa.

[22] Kenaka Yoswa anayitanitsa Agibiyoni aja nawafunsa kuti, "Chifukwa chiyani inu munatinyenga ponena kuti mumachokera kutali pamene
zoona zake n'zoti mumakhala pafupi pomwe pano? [23] Tsopano popeza mwachita izi, Mulungu wakutembererani ndipo palibe wina mwa inu amene akhale mfulu. Nthawi zonse inu muzidzatidulira nkhuni ndi kutitungira madzi ku Nyumba ya Yehova."

[24] Iwo anayankha Yoswa kuti, "Ife akapolo anufe tinachita zimenezi chifukwa tinamva bwino lomwe kuti Yehova Mulungu wanu analamula Mose mtumiki wake kuti adzakupatsani dziko lonseli ndi kuti anthu onse okhalamo adzaphedwe. Tsono ife tinachita mantha aakulu ndipo tinachita
zimenezi pofuna kupulumutsa miyoyo yathu. [25] Tsopanotu ife tili m'manja mwanu, ndipo inu chitani nafe monga kukukomerani."

[26] Tsono Yoswa anawapulumutsa m'manja mwa Aisraeli ndipo
sanawaphe. [27] Kuyambira tsiku limenelo Agibiyoni aja anasanduka odula nkhuni zaguwa lansembe la Yehova ndiponso otunga madzi. Mpaka lero lino iwo akuchitabe zimenezi kulikonse kumene Yehova anasankha.

# 10

*Kuyimitsidwa kwa Dzuwa*

[1] Adoni-Zedeki mfumu ya ku Yerusalemu inamva kuti Yoswa wagonjetsa ndi kuwononga kotheratu mzinda wa Ai pamodzi ndi mfumu yake, monga anachitira ndi Yeriko ndi mfumu yake. Inamvanso kuti anthu a ku Gibiyoni anachita pangano la mtendere ndi Israeli ndipo amakhala
pakati pawo. [2] Choncho iye ndi anthu ake anachita mantha aakulu, chifukwa Gibiyoni unali mzinda waukulu kwambiri, monga mzinda uliwonse wokhala ndi mfumu. Unali waukulu ndipo ankhondo ake anali
olimba mtima. [3] Chotsatira chake Adoni-Zedeki mfumu ya Yerusalemu inatuma uthenga kwa Hohamu mfumu ya Hebroni, Piramu mfumu ya
Yarimuti, Yafiya mfumu ya Lakisi ndi Debri mfumu ya Egiloni. [4] Iye
anatumiza mawu kuti, "Bwerani mudzandithandize kumenyana ndi Gibiyoni, chifukwa anthu ake achita pangano la mtendere ndi Yoswa ndi Aisraeli."

[5] Mafumu asanu a Aamori aja, mfumu ya Yerusalemu, mfumu ya Hebroni, mfumu ya Yarimuti, mfumu ya Lakisi ndi mfumu ya Egiloni, anagwirizana. Iwo anasonkhanitsa ankhondo awo nazungulira mzinda wa Gibiyoni ndi kuwuthira nkhondo.

[6] Koma anthu a ku Gibiyoni anatumiza uthenga kwa Yoswa ku misasa ya ku Giligala nati, "Musawataye anthu anu! Bwerani msanga mudzatipulumutse! Dzatithandizeni chifukwa mafumu a Aamori ochokera ku dziko la ku mapiri agwirizana kuti adzatithire nkhondo."

7 Choncho Yoswa ananyamuka kuchoka ku Giligala ndi gulu lake la
ankhondo pamodzi ndi anthu ake olimba mtima. 8 Yehova anati kwa
Yoswa, “Usawaope, Ine ndawapereka m’dzanja lako. Palibe ndi mmodzi
mwa amenewa amene adzalimbe.”
9 Atayenda usiku wonse kuchokera ku Giligala, Yoswa anawathira
nkhondo mwadzidzidzi. 10 Yehova anachititsa mantha adani aja atan-
goona gulu lankhondo la Israeli. Choncho Aisraeli anagonjetsa Aamori ku
Gibiyoni ndipo anawathamangitsa mu msewu wopita ku Beti-Horoni ndi
kuwapha njira yonse yopita ku Azeka ndi Makeda. 11 Pamene ankathawa
pamaso pa Israeli pa njira yochokera ku Beti-Horoni mpaka ku Azeka,
Yehova anawagwetsera matalala akuluakulu kuchokera kumwamba ndipo
ambiri mwa iwo anafa ndi matalala kuposa amene anaphedwa ndi
lupanga la Israeli.
12 Pa tsiku limene Yehova anapereka Aamori m’manja mwa Israeli,
Yoswa ananena kwa Yehova pamaso pa Israeli kuti,
“Iwe dzuwa, ima pamwamba pa Gibiyoni,
mwezi ima pamwamba pa chigwa cha Ayaloni.”
13 Choncho dzuwa linayima,
mwezinso unayima,
mpaka dziko la Israeli litagonjetsa adani ake.
Zimenezi zalembedwa m’buku la Yasari.
Dzuwa linayima pamodzimodzi pakati pa thambo mlengalenga, osayen-
danso kwa tsiku lathunthu. 14 Sipanakhaleponso tsiku ngati limeneli
kuyambira kale, tsiku limene Yehova anamvera munthu. Izi zinatero
chifukwa Yehova ankamenyera nkhondo Aisraeli.
15 Kenaka Yoswa anabwerera pamodzi ndi Aisraeli onse ku misasa ku
Giligala.

### *Kuphedwa kwa Mafumu Asanu a Aamori*

16 Mafumu asanu aja anathawa ndi kukabisala ku phanga la Makeda.
17 Koma Yoswa anamva kuti mafumu asanu awapeza akubisala ku phanga
la Makeda. 18 Tsono Yoswa analamula kuti, “Mugubuduzire miyala
ikuluikulu pa khomo la phangalo, ndipo muyike anthu ena kuti azilondera.
19 Koma inu musakhaleko! Thamangitsani adani anu, muwathire nkhondo
kuchokera kumbuyo ndipo musawalole kuti akafike ku mizinda yawo,
pakuti Yehova Mulungu wanu wawapereka m’manja mwanu.”
20 Kotero Yoswa ndi Aisraeli anapha anthu aja, kupatulapo ochepa
amene anathawa nakabisala ku mizinda yawo. 21 Kenaka gulu lonse la
ankhondo linabwerera bwinobwino kwa Yoswa ku misasa ya ku Makeda,
palibe aliyense mu mzindamo amene anaputanso Aisraeli.
22 Yoswa anati, “Tsekulani khomo la phangalo ndipo muwabweretse kwa
ine mafumu asanuwo.” 23 Pamenepo mafumu asanu aja anatulutsidwa,
mfumu ya ku Yerusalemu, mfumu ya ku Hebroni, mfumu ya ku Yarimuti,
mfumu ya ku Lakisi, ndi mfumu ya ku Egiloni. 24 Atabwera nawo kwa
Yoswa, iye anayitana Aisraeli onse. Ndipo analamula akuluakulu ake
amene anapita naye limodzi kuti, “Bwerani kuno ndipo apondeni pakhosi
mafumuwa.”
25 Yoswa anawawuza kuti, “Musaope kapena kutaya mtima. Khalani
amphamvu ndi olimba mtima popeza umo ndi mmene Yehova adzachitire
ndi adani anu onse amene mudzamenyana nawo.” 26 Kenaka Yoswa
anawabaya ndi kuwapha mafumuwo ndipo anawapachika pa mitengo
isanu ndipo anakhala pamenepo mpaka madzulo.

27 Dzuwa litalowa, Yoswa analamula kuti awachotse pa mitengo ija
ndi kuwaponya m'phanga limene ankabisalamo. Pa khomo pa phangalo
anayikapo miyala ikuluikulu imene ilipo mpaka lero.

28 Tsiku lomwelo Yoswa analanda mzinda wa Makeda. Iye anapha anthu
a mu mzindamo ndi mfumu yake ndipo sanasiye aliyense wamoyo. Yoswa
anachita ndi mfumu ya ku Makeda monga anachitira ndi mfumu ya Yeriko.

### *Agonjetsa Mizinda ya Kummwera*

29 Kenaka Yoswa ndi Aisraeli onse anapitirira kuchokera ku Makeda
nakafika ku Libina ndi kuthira nkhondo mzindawo. 30 Yehova
anaperekanso mzindawo ndi mfumu yake m'manja mwa Aisraeli. Ndipo
Yoswa anapha onse amene anali mu mzindamo. Palibe amene anatsala
wamoyo. Ndipo Yoswa anachita ndi mfumu ya Libina monga anachitira
ndi mfumu ya Yeriko.

31 Kenaka Yoswa ndi Aisraeli onse anapitirira kuchokera ku Libina
kupita ku Lakisi. Iye anazungulira mzindawo ndi kuwuthira nkhondo.
32 Yehova anapereka Lakisi kwa Israeli; ndipo Yoswa anawulanda pa
tsiku lachiwiri. Monga anachita ndi mzinda wa Libina, Yoswa anapha
anthu onse okhala mu mzinda wa Lakisi, ndipo palibe amene anatsala
ndi moyo. 33 Nthawi imeneyi n'kuti Horamu mfumu ya Gezeri itabwera
kudzathandiza Lakisi koma Yoswa anamugonjetsa pamodzi ndi asilikali
ake ndipo palibe anatsala wamoyo.

34 Kenaka Yoswa ndi Aisraeli onse anapitirira kuchokera ku Lakisi
nakafika ku Egiloni. Iwo anazungulira mzindawo ndi kuwuthira nkhondo.
35 Anawulanda tsiku lomwelo ndipo anapha aliyense amene anali mu
mzindawo monga momwe anachitira ku Lakisi.

36 Kenaka Yoswa ndi Aisraeli onse anachoka ku Egiloni nakafika ku
Hebroni ndi kukawuthira nkhondo. 37 Iwo analanda mzindawo napha
ndi lupanga mfumu yake pamodzi ndi onse amene ankakhala m'menemo.
Monga anachita ndi mzinda wa Egiloni, kuti sanasiye aliyense ndi moyo,
anachitanso chimodzimodzi ndi mzinda wa Hebroni.

38 Pambuyo pake Yoswa ndi Aisraeli onse anatembenukira mzinda wa
Debri ndi kukawuthira nkhondo. 39 Iwo analanda mzindawo ndi midzi
ndi kupha mfumu yake pamodzi ndi onse okhala m'menemo. Anachita ndi
mzinda wa Debri pamodzi ndi mfumu yake zofanana ndi zimene anachita
ndi mzinda wa Libina ndi wa Hebroni.

40 Motero Yoswa anagonjetsa dziko lonselo. Anapha mafumu onse a
dera la kumapiri, dera la kummawa, dera la kumadzulo m'mphepete
mwa phiri, ndiponso dera la ku magomo, kummwera. Iye sanasiye
wina aliyense wamoyo. Anapha onse amene anali moyo monga momwe
Yehova Mulungu wa Israeli analamulira. 41 Yoswa anawagonjetsa iwo
kuyambira ku Kadesi Barinea mpaka ku Gaza, ndiponso kuchokera ku
chigawo chonse cha Goseni mpaka ku Gibiyoni. 42 Yoswa anagonjetsa
mafumu onsewa ndi kulanda dziko lawo kamodzin'kamodzi chifukwa
Yehova Mulungu wa Israeli anawamenyera nkhondo.

43 Pambuyo pake Yoswa ndi Aisraeli onse anabwerera ku misasa yawo
ku Giligala.

# 11

### *Kugonjetsedwa kwa Mafumu a Kumpoto*

1 Yabini, mfumu ya Hazori, inamva zimene zinachitikazi. Tsono
inatumiza uthenga kwa Yobabu mfumu ya Madoni, ndiponso kwa mafumu
a ku Simironi ndi Akisafu. 2 Inatumizanso uthenga kwa mafumu a
kumpoto, kumapiri, ndi m'chigwa cha Yorodani kummwera kwa nyanja
ya Kinereti, ndiponso kumadzulo m'mbali mwa nyanja pafupi ndi Dori.
3 Inatumizanso uthenga kwa Akanaani amene ankakhala kummawa ndi
kumadzulo kwa Yorodani. Uthenga unapitanso kwa Aamori, Ahiti, Aperezi
ndi Ayebusi amene amakhala m'dziko la ku mapiri ndiponso kwa Ahivi
amene ankakhala m'munsi mwa phiri la Herimoni ku chigwa cha Mizipa.
4 Mafumuwo anabwera pamodzi ndi ankhondo awo onse. Gulu la
ankhondo linali lalikulu ngati mchenga wa m'mbali mwa nyanja. Analinso
ndi akavalo ndi magaleta ambiri. 5 Mafumu onsewa anasonkhana
pamodzi ndipo anamanga misasa yawo ku mtsinje wa Meromu, kuti
amenyane ndi Israeli.

6 Yehova anati kwa Yoswa, "Usawaope chifukwa mawa nthawi ngati
yomwe ino ndidzawapereka kuti muwaphe. Akavalo awo muwadule
matsinde ndipo magaleta awo muwatenthe ndi moto."

7 Kotero Yoswa pamodzi ndi gulu lonse la nkhondo anafika kwa adani
awo aja ku mtsinje wa Meromu modzidzimutsa ndi kuwathira nkhondo.
8 Yehova anawapereka m'manja mwa Israeli mwakuti anawagonjetseratu
ndi kuwapirikitsa njira yonse mpaka ku Sidoni Wamkulu ndi ku Misirefoti
Maimu, ndiponso kummawa ku chigwa cha Mizipa. Onse anaphedwa
popanda wopulumuka. 9 Yoswa anawachita zimene Yehova analamula.
Iye anadula matsinde a akavalo awo ndi kutentha magaleta awo.

10 Pambuyo pake Yoswa anabwera nalanda mzinda wa Hazori ndi kupha
mfumu yake. (Nthawi imeneyo mzinda wa Hazori unali wopambana
mizinda ina yonse). 11 Anapha aliyense wa mu mzindamo popanda
wotsala wamoyo, ndipo mzinda wa Hazori anawutentha ndi moto.

12 Yoswa analanda mizinda yonse ndi mafumu ake. Anthu onse
anaphedwa ndi lupanga monga momwe analamulira Mose, mtumiki wa
Yehova. 13 Israeli sanatenthe mizinda yomangidwa pa zitunda, kupatula
mzinda wa Hazori, umene Yoswa anawutentha. 14 Aisraeli anatenga
zinthu zonse za m'mizindayi pamodzi ndi ziweto kuti zikhale zawo, koma
anapha anthu onse ndi lupanga osasiyako ndi mmodzi yemwe wamoyo.
15 Monga momwe Yehova analamulira mtumiki wake Mose, nayenso Mose
analamulira Yoswa ndipo Yoswa anachita chilichonse chimene Yehova
analamulira Mose.

16 Kotero Yoswa analanda dziko lonse: dziko la ku mapiri, dera lonse
la Negevi, chigawo chonse cha Goseni, ndi chigwa chake chonse, chigwa
cha Yorodani, dziko lonse la lamapiri la Israeli pamodzi ndi chigwa chake
chomwe. 17 Dziko lolandidwalo linayambira ku phiri la Halaki limene
linali ku Seiri mpaka ku Baala-Gadi m'chigwa cha Lebanoni, kumunsi
kwa phiri la Herimoni. Yoswa anagwira ndi kupha mafumu a dziko
lonselo 18 atachita nawo nkhondo kwa nthawi yayitali. 19 Palibe ngakhale
ndi mfumu imodzi yomwe imene inachita mgwirizano wa mtendere ndi
Aisraeli kupatula Ahivi okhala ku Gibiyoni. Koma mizinda ina yonse
anachita kuyigonjetsa pa nkhondo. 20 Yehova anali atawumitsa mitima
yawo kuti alimbane ndi Aisraeli kuti aphedwe popanda kuchitiridwa
chifundo. Izi ndi zimene Yehova analamula Mose kuti zichitidwe.

21 Pa nthawi imeneyi Yoswa anapita kukawononga Aanaki okhala
m'dziko lija la ku mapiri ku Hebroni, Debri, Anabu komanso madera onse

a ku mapiri a Yuda ndi Israeli. Yoswa anawawononga onse pamodzi ndi
mizinda yawo. 22 Palibe ndi mmodzi yemwe amene anatsalako m'dziko
lonse la Israeli; komabe ku Gaza, ku Gati ndi Asidodi kokha ndi kumene
anatsalako pang'ono. 23 Choncho Yoswa anagonjetsa dziko lonse monga
momwe Yehova analamulira Mose. Tsono Yoswa analipereka kwa Aisraeli
kuti likhale lawo, fuko lililonse gawo lake.

Anthu onse anapumula, osamenyanso nkhondo.

# 12

### *Mayina a Mafumu Ogonjetsedwa*

1 Aisraeli anagonjetsa dziko lonse la kummawa kwa Yorodani, kuyambira ku chigwa cha Arinoni mpaka ku phiri la Herimoni pamodzi ndi dera lonse la kummawa kwa Araba. Iwo anatenga dzikoli kukhala lawo, ndipo mafumu a dzikoli anali awa:

2 Sihoni mfumu ya Aamori,
amene ankakhala mu Hesiboni. Iye analamulira kuyambira ku Aroeri
mzinda umene uli m'mphepete mwa mtsinje wa Arinoni, mpaka ku
mtsinje wa Yaboki, umene uli m'malire mwa Aamori, kuphatikizanso
theka la dziko la Giliyadi. 3 Iye ankalamuliranso dera la chigwa cha
Yorodani kuyambira ku Nyanja ya Kinereti, kummawa ndi kumatsika
mpaka ku Beti-Yesimoti, mzinda umene unali kummawa kwa Nyanja ya
Mchere ndi kutsikabe kummwera mpaka pa tsinde pa phiri la Pisiga.

4 Ogi mfumu ya mzinda wa Basani,
amene anali mmodzi mwa otsala mwa Arefaimu. Iye ankakhala ku
Asiteroti ndi Ederi. 5 Dera la ufumu wake linafika ku phiri la Herimoni,
ku Saleka ndi dziko lonse la Basani mpaka ku malire ndi anthu a ku
Gesuri Makati. Ufumu wake unaphatikizanso theka la Giliyadi mpaka
ku malire a mfumu Sihoni ya ku Hesiboni.

6 Mose mtumiki wa Yehova ndi Aisraeli anawagonjetsa ndipo anapereka dziko lawo kwa anthu a fuko la Rubeni, fuko la Gadi ndi theka la fuko la Manase kuti chikhale cholowa chawo.

7 Yoswa ndi Aisraeli onse anagonjetsa mafumu onse okhala kumadzulo
kwa mtsinje wa Yorodani kuyambira ku Baala-Gadi, ku chigwa cha
Lebanoni mpaka ku phiri la Halaki, kumapita cha ku Seiri. Yoswa
anagawira dzikolo mafuko a Israeli kuti likhale cholowa chawo. 8 Dziko
limeneli linali dera la ku mapiri, chigwa cha kumadzulo, chigwa cha
Yorodani, ku matsitso a kummawa, ndi dziko la chipululu la kummwera.
Amene ankakhala m'dzikoli anali Ahiti, Aamori, Akanaani, Aperezi, Ahivi
ndi Ayebusi. Mafumu ake anali awa:

| | |
|---|---|
| 9 mfumu ya Yeriko | imodzi |
| mfumu ya Ai (kufupi ndi Beteli | imodzi |
| 10 mfumu ya Yerusalemu | imodzi |
| mfumu ya Hebroni | imodzi |
| 11 mfumu ya Yarimuti | imodzi |
| mfumu ya Lakisi | imodzi |
| 12 mfumu ya Egiloni | imodzi |
| mfumu ya Gezeri | imodzi |
| 13 mfumu ya Debri | imodzi |
| mfumu ya Gederi | imodzi |
| 14 mfumu ya Horima | imodzi |
| mfumu ya Aradi | imodzi |
| 15 mfumu ya Libina | imodzi |
| mfumu ya Adulamu | imodzi |
| 16 mfumu ya Makeda | imodzi |
| mfumu ya Beteli | imodzi |
| 17 mfumu ya Tapuwa | imodzi |
| mfumu ya Heferi | imodzi |
| 18 mfumu ya Afeki | imodzi |
| mfumu ya Lasaroni | imodzi |
| 19 mfumu ya Madoni | imodzi |
| mfumu ya Hazori | imodzi |
| 20 mfumu ya Simuroni Meroni | imodzi |
| mfumu ya Akisafu | imodzi |
| 21 mfumu ya Taanaki | imodzi |
| mfumu ya Megido | imodzi |
| 22 mfumu ya Kadesi | imodzi |
| mfumu ya Yokineamu ku Karimeli | imodzi |
| 23 mfumu ya Dori ku Nafoti Dori | imodzi |
| mfumu ya Goyini ku Giligala | imodzi |
| 24 mfumu ya Tiriza | imodzi |
| | mafumu onse pamodzi analipo 31. |

# 13

*Mayiko Otsala Oyenera Kulandidwa*

1 Yoswa atakalamba Yehova anamuwuza kuti, Iwe tsopano wakalamba kwambiri, koma dziko losalandidwa lilipobe lalikulu.

2 "Madera amene atsala ndi awa: chigawo chonse cha Afilisti ndi Agesuri
3 kuchokera ku mtsinje wa Sihori kummawa kwa Igupto mpaka kumpoto
kwa dziko la Ekroni. Madera onse amawerengedwa kuti ndi a Akanaani
ngakhale amalamulidwa ndi mafumu asanu a Afilisti a ku Gaza, Asidodi,
Asikeloni, Gati, Ekroni ndi Agiti, komanso ku Avimu ku chigawo cha
kumpoto. 4 Dziko lina la Akanaani ndi Ameara limene lili m'manja mwa
Asidoni mpaka ku Afeki, dziko limene linachitana malire ndi dziko la
Aamori. 5 Palinso dziko lonse la Gebala ndi Lebanoni cha kummawa

kuyambira ku Baala-Gadi pa tsinde pa phiri la Herimoni mpaka ku Lebo Hamati.

6 "Palinso anthu okhala m'chigawo cha ku mapiri kuchokera ku Lebanoni mpaka ku Misirefoti-Maimu, Ine ndidzawapirikitsa pamene Aisraeli azidzalowa. Tsono uwagawire Aisraeli dziko limeneli kuti likhale
cholowa chawo monga momwe ndakulamulira. 7 Tsopano ugawire dziko
limeneli mafuko asanu ndi anayi ndiponso theka la fuko la Manase, kuti likhale cholowa chawo."

### *Kugawidwa kwa Dziko la Kummawa kwa Yorodani*

8 Anthu a fuko la Rubeni ndi fuko la Gadi pamodzi ndi theka lina la fuko la Manase analandira kale cholowa chawo chimene Mose mtumiki wa Yehova anawapatsa. Cholowa chawocho chinali kummawa kwa mtsinje wa Yorodani.

9 Dziko lawolo linayambira ku Aroeri mzinda umene uli pafupi ndi chigwa cha Arinoni, ndiponso mzinda umene uli pakati pa chigwacho. Dzikolo linkaphatikizanso dera lonse lokwera kuyambira ku Medeba
mpaka ku Diboni. 10 Linkaphatikizanso mizinda yonse ya mfumu Sihoni ya Aamori, imene inkalamulira mu Hesiboni, mpaka ku malire
a Aamoni. 11 Dzikoli linaphatikizanso Giliyadi, dziko la anthu a ku Gesuri ndi Maaka, phiri lonse la Herimoni ndi dziko lonse la Basani
mpaka ku Saleka. 12 Linaphatikizanso dziko la mfumu Ogi ya ku Basani imene imalamulira kuchokera ku Asiteroti ndi Ederi. Iye yekha ndiye anali mfumu ya Arefaimu amene anapulumuka. Mose anali
atawagonjetsa anthu amenewa ndi kuwathamangitsira kutali. 13 Koma
Aisraeli sanathamangitse anthu a ku Gesuri ndi Maaka, kotero iwowa amakhalabe pakati pawo mpaka lero.

14 Koma Mose sanapereke dziko kwa fuko la Alevi popeza zopereka zopatulika zimene anthu ankapereka kwa Yehova, Mulungu wa Israeli, ndizo zinali cholowa chawo monga Yehova anawalonjezera.

15 Mose anapereka gawo lina la dziko kwa mabanja a fuko la Rubeni.

16 Dziko lawo linayambira ku Aroeri mzinda umene uli pafupi ndi chigwa cha Arinoni, m'mudzi wa pakati pa chigwa, ndiponso dera
lonse lokwera mpaka ku Medeba. 17 Dzikolo linaphatikizanso Hesiboni
ndi mizinda yake yonse, komanso mizinda monga Diboni, Bamoti
Baala, Beti-Baala-Meoni, 18 Yahaza, Kedemoti, Mefaati. 19 Kiriataimu,
Sibima, Zereti-Sahari, pa phiri limene lili m'chigwa, 20 Beti-Peori, ku
matsitso a Pisiga, ndiponso Beti-Yesimoti. 21 Dzikolo linaphatikizanso
mizinda yonse ya ku madera okwera ndiponso dziko lonse la mfumu Sihoni ya Aamori amene ankalamulira kuchokera ku Hesiboni. Mose anamugonjetsa iye pamodzi ndi mafumu a Amidiyani awa: Evi, Rekemu, Zuri, Huri ndi Reba, mafumu amene anagwirizana ndi Sihoni. Onsewa
analamulira dzikolo ngati nduna za Sihoni. 22 Kuwonjezera pa amene
anaphedwa ndi nkhondo, Aisraeli anapha ndi lupanga Balaamu mwana
wa Beori, amene amachita za matsenga. 23 Malire a fuko la Rubeni
anali mtsinje wa Yorodani. Mizinda imeneyi pamodzi ndi midzi yake zinapatsidwa kwa mabanja a fuko la Rubeni kuti akhale cholowa chawo.

24 Dera limene Mose anapereka kwa mabanja a fuko la Gadi ndi ili:

25 Dziko la Yazeri, mizinda yonse ya mu Giliyadi ndiponso theka la dziko
la Amori kukalekezera ku Aroeri, kufupi ndi Raba; 26 ndiponso kuyam-
bira ku Hesiboni mpaka ku Ramati-Mizipa, ndi Betonimu; ndiponso
kuyambira ku Mahanaimu mpaka ku dziko la Debri. 27 Mu chigwa
cha Yorodani analandiramo Beti-Haramu, Beti-Nimira, Sukoti ndi Zafoni
pamodzi ndi dziko lonse la mfumu Sihoni ya ku Hesiboni. Malire ake a
ku madzulo anali mtsinje wa Yorodani kufikira ku Nyanja ya Kinereti,
kumpoto. 28 Mizinda ndi midzi imeneyi inali cholowa cha mabanja a
fuko la Gadi.

29 Mose anali atapereka kale gawo lina la dziko limeneli kwa theka la
mabanja a fuko la Manase kuti likhale cholowa chawo.
30 Derali linayambira ku Mahanaimu kuphatikizapo dziko lonse la
mfumu Ogi, Mfumu ya ku Basani, pamodzi ndi mizinda 60 ya ku Yairi,
ku Basaniko. 31 Derali linaphatikizanso theka la Giliyadi pamodzi ndi
Asiteroti ndi Ederi, mizinda yayikulu ya mfumu Ogi wa Basani. Mizinda
imeneyi inapatsidwa kwa mabanja a Makiri, mwana wa Manase kuti
ikhale cholowa cha theka la ana a Makiri, malinga ndi mabanja awo.

32 Umu ndi mmene Mose anagawira malo a m'chigwa cha Yorodani,
kummawa kwa Yeriko, ku tsidya kwa Yorodani. 33 Komatu Mose
sanapereke malo kwa fuko la Levi. Mose anawawuza kuti zopereka
zimene anthu ankapereka kwa Yehova ndizo cholowa chawo.

# 14

### *Kugawa kwa Dziko la Kumadzulo kwa Yorodani*

1 Umu ndi mmene Aisraeli analandirira cholowa chawo m'dziko la
Kanaani. Eliezara wansembe, Yoswa mwana wa Nuni pamodzi ndi
akuluakulu a mafuko a Israeli ndiwo anagawa dzikolo kugawira Aisraeli.
2 Madera anagawidwa mwa maere kwa mafuko asanu ndi anayi ndi
theka, monga momwe Yehova analamulira kudzera mwa Mose. 3 Mose
anapereka kwa mafuko awiri ndi theka dziko la kummawa kwa Yoro-
dani, koma fuko la Levi lokha silinagawiridwe malo. 4 Tsono fuko la
Yosefe analigawa pawiri, Manase ndi Efereimu. Mose sanawagawire
malo mabanja a fuko la Levi, koma iwo anangolandira mizinda imene
ankakhalamo pamodzi ndi malo amene ankawetako nkhosa ndi ng'ombe
zawo. 5 Choncho Aisraeli anagawana dzikolo, monga momwe Yehova
analamulira Mose.

### *Apereka Hebroni kwa Kalebe*

6 Tsono anthu a fuko la Yuda anabwera kwa Yoswa ku Giligala, ndipo
Kalebe mwana wa Yefune Mkeni anati kwa iye, "Inu mukudziwa zimene
Yehova ananena kwa Mose munthu wa Mulungu za inu ndi ine ku Kadesi
Barinea. 7 Nthawi imene Mose mtumiki wa Yehova ananditumа kuchokera
ku Kadesi Barinea kudzayendera dzikoli ndinali ndi zaka makumi anayi.
Ndipo nditabwerako ndinamuwuza zoona zokhazokha monga momwe
ndinaonera. 8 Koma abale anga amene ndinapita nawo anachititsa anthu
mantha. Komabe ine ndinamvera Yehova Mulungu wanga ndi mtima
wonse. 9 Kotero tsiku limenelo Mose anandilonjeza kuti, 'Dziko limene
unayendamo lidzakhala lako ndiponso la ana ako kwamuyaya chifukwa
unamvera Yehova Mulungu wanga ndi mtima wako wonse.'

10 "Tsono papita zaka 45 chiyankhulire Yehova zimenezi kwa Mose.
Nthawi imeneyo n'kuti Aisraeli akuyendayenda m'chipululu. Yehova
wandisunga ndipo tsopano ndili ndi zaka 85. 11 Komabe ndikanali ndi
mphamvu lero, monga ndinalili tsiku lija Mose ananditurna. Ndili ndi
mphamvu moti ndikhoza kupita ku nkhondo kapena kuchita kanthu
kena kalikonse. 12 Tsopano ndipatseni dziko la ku mapiri limene Yehova
anandilonjeza tsiku lija. Inu munamva nthawi ija kuti Aanaki anali
kumeneko ndipo kuti mizinda yawo inali ikuluikulu ndi yotetezedwa.
Komabe Yehova atakhala nane ndidzawathamangitsa monga Iye ananen-
era."
13 Ndipo Yoswa anadalitsa Kalebe mwana wa Yefune ndi kumupatsa
Hebroni kukhala dziko lake. 14 Choncho dera la Hebroni lakhala lili la
Kalebe mwana wa Yefune Mkeni mpaka lero chifukwa anamvera Yehova
Mulungu wa Israeli ndi mtima wonse. 15 (Hebroni ankatchedwa Kiriati
Ariba chifukwa cha Ariba amene anali munthu wamphamvu kwambiri
pakati pa Aanaki).
Ndipo kenaka m'dziko monse munakhala mtendere.

# 15

*Dziko Limene Yuda Analandira*

1 Chigawo cha dzikolo chimene mabanja a fuko la Yuda analandira
chinafika ku malire ndi Edomu mpaka ku chipululu cha Zini kummwera
kwenikweni.
2 Malire awo a kummwera anayambira kummwera kwenikweni kwa
Nyanja ya Mchere, 3 kudutsa cha kummwera ku Akirabimu, n'kupitirira
mpaka ku Zini. Kuchokera pamenepo n'kumapita cha kummwera kwa
Kadesi Barinea, kudutsa Hezironi mpaka ku Adari ndi kutembenuka
mpaka ku Karika. 4 Anapitirira mpaka ku Azimoni motsata mtsinje
umene uli malire a Igupto mpaka ku nyanja. Awa ndiwo malire awo
a kummwera.
5 Malire a kummawa anali Nyanja Yakufa mpaka kumene Yorodani
amathira mu Nyanja ya Mchere.
Malire a kumpoto anayambira kumene Yorodani amathirira nyanjayo,
6 napitirira mpaka ku Beti-Hogila ndi kupitirira kumpoto mpaka ku Beti-
Araba. Anapitirira mpaka anakafika ku Mwala wa Bohani. 7 Ndipo
malirewo anachokeranso ku chigwa cha Akori mpaka ku Debri, ku-
chokera ku chigwa cha Akori ndi kutembenukira kumpoto ku Giligala,
dera limene linayang'anana ndi msewu wa Adumimu kummwera kwa
chigwa. Anapitirira mpaka ku madzi a ku Eni Semesi ndi kutulukira
ku Eni Rogeli. 8 Ndipo anapitirira mpaka ku chigwa cha Hinomu
mbali ya kummwera kwa mzinda wa Ayebusi (mzinda wa Yerusalemu).
Kuchokera kumeneko anakwera mpaka pamwamba pa phiri kumadzulo
kwa chigwa cha Hinomu cha kumpoto kwenikweni kwa chigwa cha
Refaimu. 9 Ndipo anachokeranso pamwamba pa phiri, kukafika mpaka
ku akasupe a ku Nepitowa, nadzatulukira ku mizinda ya phiri la
Efroni, ndi kutsikira ku Baalahi (ndiye Kiriati Yearimu). 10 Kuchokera
kumeneko anazungulira cha kumadzulo ku Baalahi mpaka ku phiri la
Seiri. Anapitirira cha kumpoto kutsata phiri la Yearimu (lomwe ndi
Kesaloni). Anapitirirabe kutsika ku Beti Semesi ndi kuwolokera ku
Timna. 11 Malirewo anapitirira kumatsitso a mapiri chakumpoto kwa
Ekroni, ndi kukhotera ku Sikeroni. Malirewo anadutsa phiri la Baalahi
ndi kufika ku Yabineeli. Malirewo anathera ku nyanja.

12 Malire a mbali ya kumadzulo anali Nyanja Yayikulu.

Awa ndi malire ozungulira malo amene anapatsidwa kwa mabanja a fuko
la Yuda.

13 Potsata lamulo la Yehova, Yoswa anapereka kwa Kalebe mwana wa
Yefune gawo lina la dziko la Yuda dera la Kiriati Ariba, limene ndi
Hebroni. (Ariba anali gogo wa Aanaki). 14 Kuchokera ku Hebroni, Kalebe
anathamangitsamo mafuko a Aanaki awa: Sesai, Ahimani ndi Talimai,
zidzukulu za Aanaki. 15 Kuchokera kumeneko, Kalebe anakathira nkhondo
anthu amene ankakhala ku Debri (mzindawu poyamba unkatchedwa
Kiriati Seferi). 16 Tsono Kalebe anati, "Munthu amene angathire nkhondo
mzinda wa Kiriati Seferi ndi kuwulanda, ndidzamupatsa mwana wanga
Akisa kuti akhale mkazi wake." 17 Otanieli, mwana wa m'bale wa Kalebe,
Kenazi, ndiye anawulanda. Choncho Kalebe anamupatsa mwana wake
Akisa kuti akhale mkazi wake.
18 Tsiku lina atafika Akisayo, Otanieli anamuwumiriza mkazi wakeyo
kuti apemphe munda kwa Kalebe abambo ake. Pamene Akisa anatsika pa
bulu wake, Kalebe anamufunsa kuti, "Kodi ukufuna ndikuchitire chiyani."
19 Iye anayankha kuti "Mundikomere mtima. Popeza mwandipatsa ku
Negevi, kumalo kumene kulibe madzi, mundipatsenso akasupe amadzi."
Choncho Kalebe anamupatsa akasupe a kumtunda ndi a kumunsi.

20 Dziko limene mabanja a fuko la Yuda analandira ngati cholowa chawo
ndi ili:

21 Mizinda yakummwera kwenikweni kwa fuko la Yuda yoyandikana ndi
malire a Edomu anali:
Kabizeeli, Ederi, Yaguri 22 Kina, Dimona, Adada 23 Kedesi, Hazori,
Itinani 24 Zifi, Telemu, Bealoti, 25 Hazori-Hadata, Keriyoti Hezironi (ndiye
kuti Hazori) 26 Amamu, Sema, Molada 27 Hazari-Gada, Hesimoni, Beti-
Peleti 28 Hazari-Suwali, Beeriseba, Biziotiya, 29 Baalahi, Iyimu, Ezemu
30 Elitoladi, Kesili, Horima 31 Zikilagi, Madimena, Sanisana, 32 Lebaoti,
Silihimu, Aini ndi Rimoni. Mizinda yonse inalipo 29 pamodzi ndi midzi
yake yozungulira.

33 Mizinda ya ku chigwa cha kumadzulo ndi iyi:
Esitaoli, Zora, Asina 34 Zanowa, Eni-Ganimu, Tapuwa, Enamu,
35 Yarimuti, Adulamu, Soko, Azeka, 36 Saaraimu, Aditaimu, ndi Gederi
(kapena Gederotaimu). Mizinda yonse inalipo 14 pamodzi ndi midzi
yake yozungulira.
37 Mizinda ina inali iyi: Zenani, Hadasa, Migidali-Gadi, 38 Dileani,
Mizipa, Yokiteeli, 39 Lakisi, Bozikati, Egiloni, 40 Kaboni, Lahimasi, Kitilisi,
41 Gederoti, Beti-Dagoni, Naama ndi Makeda. Mizinda yonse pamodzi
inalipo 16 pamodzi ndi midzi yake yozungulira.
42 Mizinda ina inali iyi: Libina, Eteri, Asani, 43 Ifita, Asina, Nezibu,
44 Keila, Akizibu ndi Maresa, mizinda isanu ndi inayi pamodzi ndi midzi
yake.
45 Panalinso Ekroni pamodzi ndi midzi yake; 46 komanso yonse imene
inali m'mbali mwa Asidodi ndi midzi yake kuyambira ku Ekroni mpaka
ku Nyanja Yayikulu. 47 Panalinso mizinda ya Asidodi ndi Gaza pamodzi

ndi midzi yawo. Malire ake anafika ku mtsinje wa Igupto mpaka ku Nyanja Yayikulu.

48 Mizinda ya kumapiri inali:
Samiri, Yatiri, Soko, 49 Dana, Kiriati-Sana, (ndiye kuti Debri) 50 Anabu,
Esitemo, Animu, 51 Goseni, Holoni ndi Gilo. Mizinda yonse pamodzi inali khumi ndi umodzi pamodzi ndi midzi yake.
52 Analandiranso mizinda iyi: Arabu, Duma, Esani, 53 Yanumu, Beti-
Tapuwa, Afeki 54 Humita, Kiriati-Ariba (ndiye kuti Hebroni) ndi Ziori, mizinda isanu ndi inayi pamodzi ndi midzi yake.
55 Panalinso Maoni, Karimeli, Zifi, Yuta 56 Yezireeli, Yokideamu,
Zanowa, 57 Kaini, Gibeya ndi Timna, mizinda khumi ndi midzi yake.
58 Mizinda ina inali: Halihuli, Beti Zuri, Gedori, 59 Maarati, Beti-Anoti ndi Elitekoni, mizinda isanu ndi umodzi pamodzi ndi midzi yake
60 Panalinso Kiriati Baala (ndiye kuti Kiriati Yearimu) ndi Raba; mizinda iwiri pamodzi ndi midzi yake.

61 Mizinda ya ku chipululu inali iyi:
Beti-Araba, Midini, Sekaka, 62 Nibisani, Mzinda wa Mchere ndi Eni Gedi, mizinda isanu ndi umodzi pamodzi ndi midzi yake.

63 Koma Yuda sanathe kuthamangitsa Ayebusi amene amakhala ku Yerusalemu, ndipo mpaka lero Ayebusi akukhala komweko pamodzi ndi Ayudawo.

# 16

*Madera amene Efereimu ndi Manase Analandira*

1 Dziko limene linapatsidwa kwa fuko la Yosefe linayambira ku mtsinje wa Yorodani ku Yeriko, kummawa kwa akasupe a Yeriko, ndiponso kuyambira mtsinje wa Yorodaniwo n'kumakwera, kudutsa m'chipululu
mpaka ku mapiri a ku Beteli. 2 Kuchokera ku Beteli malire ake anakafika
ku Luzi, kudutsa dziko la Ataroti kumene kumakhala Aariki. 3 Malirewo anatsikira cha kumadzulo kwa dziko la Yafuleti mpaka ku chigawo cha kumunsi kwa Beti-Horoni. Kuchokera kumeneko anapitirira mpaka ku Gezeri n'kuthera ku Nyanja.
4 Choncho Manase ndi Efereimu, ana a Yosefe analandira cholowa chawo.

5 Dziko la mabanja a fuko la Efereimu ndi ili:
Malire a dzikolo anachokera kummawa kwa Ataroti Adari mpaka
ku mtunda kwa Beti-Horoni. 6 Malirewo anapitirira mpaka ku nyanja.
Mikimetati anali kumpoto kwake. Kuchokera kumeneko anakhotera cha kummawa kuloza ku Taanati Silo ndi kudutsa kumeneko cha kummawa
mpaka ku Yanowa. 7 Ndipo kuchokera ku Yanowa anatsikira ku Ataroti
ndi Naara, nakafika ku Yeriko ndi kukathera ku mtsinje wa Yorodani.
8 Kuchokera ku Tapuwa anapita kumadzulo mpaka ku mtsinje wa Kana
ndi kukathera ku nyanja. Dziko ili linali cholowa cha mabanja afuko
la Efereimu, 9 kuphatikizapo mizinda yonse ndi midzi yake yopatsidwa kwa Efereimu, koma yokhala m'kati mwa dziko la Manase.
10 Iwo sanapirikitse Akanaani amene amakhala ku Gezeri ndipo mpaka lero Akanaani akukhala pakati pa Aefereimu koma amagwira ntchito ngati akapolo.

# 17

1 Gawo lina la dzikolo linapatsidwa kwa mabanja ena a fuko la
Manase, mwana woyamba kubadwa wa Yosefe. Makiri anali mwana
woyamba kubadwa wa Manase ndiponso kholo la anthu okhala ku
Giliyadi. Popeza kuti iye anali munthu wankhondo, analandira Giliyadi
ndi Basani. 2 Mabanja ena otsala a fuko la Manase amene analandira
dziko ndi awa: Abiezeri, Heleki, Asirieli, Sekemu, Heferi ndi Semida. Izi
ndi zidzukulu zina zazimuna za Manase mwana wa Yosefe ndiponso eni
mbumba.
3 Panali Zelofehadi mwana wa Heferi, mwana wa Giliyadi, mwana wa
Makiri mwana wa Manase. Iyeyu analibe ana aamuna koma aakazi
okhaokha ndipo mayina awo ndi awa: Mahila, Nowa, Hogila, Milika ndi
Tiriza. 4 Iwo anapita kwa Eliezara wansembe, Yoswa mwana wa Nuni,
ndi atsogoleri ndipo anati: "Yehova analamula Mose kuti ife ndi alongo
athu atipatse cholowa chathu." Choncho iwowo pamodzi ndi abale a
abambo awo anawapatsa dera lina la dzikolo kuti likhale monga mwa
lamulo la Yehova. 5 Choncho kuwonjezera pa mayiko a Giliyadi ndi Basani
kummawa kwa Yorodani, anthu a fuko la Manase analandiranso magawo
khumi 6 chifukwa ana aakazi a fuko la Manase analandira cholowa chawo
pakati pa ana aamuna. Dziko la Giliyadi linali dziko la zidzukulu zonse za
Manase.
7 Malire a dziko la Manase anayambira ku Aseri, ndipo anakafika ku
Mikimetati kummawa kwa Sekemu. Tsono malire anapita kummwera
kuloza kwa anthu a ku Eni-Tapuwa. 8 (Manase anatenga dziko la
Tapuwa, koma mzinda wa Tapuwawo, umene unali m'malire mwa
Manase unali wa fuko la Efereimu). 9 Ndipo malire ake anapitirira
kummwera mpaka ku mtsinje wa ku Kana. Mizinda ya kummwera
kwa mtsinjewo inali ya fuko la Efereimu ngakhale kuti inali m'dziko
la Manase. Malire a fuko la Manase anapita kumpoto kwa mtsinje wa
Kana ndi kukathera ku Nyanja. 10 Dziko la kummwera linali la Efereimu
ndipo la kumpoto linali la Manase. Dziko la Manase linafika ku nyanja
ndipo linachita malire ndi Aseri, kumpoto ndiponso Isakara, kummawa.
11 M'dziko la Isakara ndi Aseri, Manase analinso ndi mizinda ya Beti-
Seani ndi Ibuleamu pamodzi ndi midzi yawo yozungulira. Panalinso
Akanaani amene ankakhala ku Dori, Endori, Taanaki ndi Megido
pamodzi ndi mizinda yozungulira (wachitatu pa m'ndandandawu ndi
Nafati Dori).
12 Komabe anthu a fuko la Manase sanathe kuwapirikitsa anthu
okhala m'mizinda imeneyi. Choncho Akanaani anakhalabe m'mizindayi.
13 Ngakhale Aisraeli anali a mphamvu m'dzikomo, sanapirikitse Akanaani
onse koma anangowasandutsa kukhala akapolo.

14 Anthu a fuko la Yosefe anati kwa Yoswa, "Chifukwa chiyani mwati-
patsa gawo limodzi lokha la dziko kuti likhale cholowa chathu? Ife tilipo
anthu ambiri popeza Yehova watidalitsa kwambiri."
15 Yoswa anayankha kuti, "Ngati muli ambiri ndipo dziko la ku mapiri la
Efereimu lakucheperani kwambiri, lowani ku nkhalango mudule mitengo,
mudzikonzere malo akuti mukhalemo, m'dziko la Aperezi ndi Arefai."
16 Tsono zidzukulu za Yosefe zinati, "Dziko la ku mapiri ndi losatikwani-
radi, komanso Akanaani onse amene akukhala ku chigwa pamodzi ndi
amene akukhala ku Beti-Seani ndi madera awo ndiponso amene ali ku
chigwa cha Yezireeli ali ndi magaleta azitsulo."

[17] Koma Yoswa anawuza zidzukulu za Yosefe, za fuko la Efereimu
ndi za fuko la Manase kuti, “Inu mulipodi ambiri ndiponso amphamvu.
Simulandira gawo limodzi lokha, [18] dziko la ku mapiri lidzakhalanso lanu.
Ngakhale kuti ndi nkhalango yokhayokha koma inu mudzadula mitengo
yake ndipo lidzakhala lanu mpaka kumapeto. Ngakhale kuti Akanaani
ali ndi magaleta azitsulo ndiponso kuti iwo ndi amphamvu, koma inu
mudzawapirikitsa.”

# 18

### *Kugawa kwa Madera Otsala a Dziko*

[1] Atagonjetsa dziko lonse Aisraeli anasonkhana ku Silo ndipo anay-
imikako tenti ya msonkhano. [2] Koma pa nthawiyo n’kuti mafuko asanu
ndi awiri a Aisraeli asanalandire cholowa chawo.

[3] Ndipo Yoswa anati kwa Aisraeli, “Kodi mudikira mpaka liti kuti
mulowe ndi kulanda dziko limene Yehova Mulungu wa makolo anu
wakupatsani? [4] Sankhani amuna atatu kuchokera ku fuko lililonse ndipo
ine ndidzawatuma kuti akayendere dzikolo ndi kukalilembera bwino kuti
ndiligawe kukhala lawo. Akatero, abwererenso kwa ine. [5] Aligawe dzikolo
m’zigawo zisanu ndi ziwiri; fuko la Yuda lidzakhale ndi dziko lake la
kummwera ndi nyumba ya Yosefe ikhalebe m’dziko lawo la kumpoto.
[6] Mudzalembe mawu ofotokoza za zigawo zisanu ndi ziwiri za dzikolo, ndi
kubwera nawo kwa ine. Tsono ineyo ndidzakuchitirani maere pamaso pa
Yehova Mulungu wanu. [7] Alevi asakhale ndi dziko pakati panu, chifukwa
gawo lawo ndi kutumikira Yehova pa ntchito ya unsembe. Ndipo Gadi,
Rubeni ndi theka la fuko la Manase analandira kale cholowa chawo
kummawa kwa Yorodani. Mose mtumiki wa Yehova ndiye anawapatsa.”

[8] Anthuwo akupita kukalembera dzikolo, Yoswa anawalangiza kuti,
“Pitani mukayendere ndi kulembera dzikolo. Kenaka mukabwere kwa
ine, ndidzakuchitirani maere kuno ku Silo pamaso pa Yehova.” [9] Ndipo
anthu anachoka ndi kukayendera dziko lonse. Iwo analemba bwinobwino
m’buku za dzikolo, mzinda ndi mzinda. Analigawa magawo asanu ndi
awiri, ndipo anabwerera kwa Yoswa ku misasa ya ku Silo. [10] Pambuyo
pake Yoswa anawachitira maere ku Silo pamaso pa Yehova, ndipo fuko
lililonse la Israeli analigawira dziko lake.

### *Dziko la Benjamini*

[11] Maere anagwera mabanja a fuko la Benjamini. Dziko limene anapat-
sidwa linali pakati pa fuko la Yuda ndi fuko la Yosefe:

[12] Mbali ya kumpoto malire awo anayambira ku Yorodani nalow-
era chakumpoto kwa matsitso a ku Yeriko kulowera cha kumadzulo
kwa dziko la ku mapiri ndi kukafika ku chipululu cha Beti-Aveni.
[13] Kuchokera kumeneko malirewo analoza ku Luzi nadutsa m’mbali
mwa mapiri kummwera kwa Luzi (ndiye Beteli) ndipo anatsika mpaka
ku Ataroti Adari, ku mapiri a kummwera kwa Beti-Horoni wa Kumunsi.

[14] Ndipo malirewo analowanso kwina, analunjika kummwera kuchok-
era kumadzulo kwake kwa phiri loyang’anana ndi Beti-Horoni, mpaka
ku mzinda wa Kiriyati Baala (ndiye Kiriati Yearimu), mzinda wa anthu
a fuko la Yuda. Amenewa ndiye anali malire a mbali ya kumadzulo.

[15] Malire a kummwera anayambira m’mphepete mwenimweni mwa
Kiriati Yearimu napita kumadzulo mpaka kukafika ku akasupe a
Nefitowa. [16] Malire anatsikira m’mphepete mwa phiri loyang’anana

ndi chigwa cha Beni Hinomu, kumpoto kwa chigwa cha Refaimu.
Anapitirira kutsikira ku chigwa cha Hinomu kummwera kwa chitunda
cha Ayebusi mpaka ku Eni Rogeli. 17 Kenaka anakhotera kumpoto kupita
ku Eni-Semesi, kupitirira mpaka ku Geliloti amene amayang'anana ndi
pokwera pa Adumimu. Kenaka malire anatsikira ku Mwala wa Bohani,
mwana wa Rubeni. 18 Anabzola cha kumpoto kwa chitunda cha Beti
Araba ndi kutsikabe mpaka ku chigwa cha Yorodani. 19 Anabzolanso
cha kumpoto kwa chitunda cha Beti-Hogila kukafika cha kumpoto ku
gombe la Nyanja ya Mchere kumene mtsinje wa Yorodani umathirirako,
cha kummwera kwenikweni. Awa anali malire a kummwera.
20 Yorodani ndiye anali malire a mbali ya kummawa.

Awa anali malire a dziko limene mabanja a fuko la Benjamini analandira.

21 Mabanja a fuko la Benjamini anali ndi mizinda iyi;
Yeriko, Beti-Hogila, Emeki Kezizi, 22 Beti-Araba, Zemaraimu, Beteli
23 Avimu, Para, Ofiri, 24 Kefari-Amoni, Ofini ndi Geba, mizinda khumi
ndi awiri ndi midzi yake
25 Panalinso Gibiyoni, Rama, Beeroti, 26 Mizipa, Kefira, Moza
27 Rekemu, Iripeeli, Tarala, 28 Zera Haelefu, mzinda wa Ayebusi (ndiye
kuti Yerusalemu) Gibeya ndi Kiriati, mizinda 14 ndi midzi yake.

Limeneli ndilo dziko limene mabanja a fuko la Benjamini analandira kuti likhale lawo.

# 19

*Dziko la Simeoni*

1 Maere achiwiri anagwera mabanja a fuko la Simeoni. Dziko lawo linali
m'kati mwenimweni mwa dziko la Yuda. 2 Dzikolo linaphatikiza zigawo
izi:
Beeriseba (ndi Seba), Molada, 3 Hazari-Suwali, Bala, Ezemu, 4 Elitoladi,
Betuli, Horima, 5 Zikilagi, Beti-Marikaboti, Hazari-Susa, 6 Beti-Lebaoti ndi
Saruheni. Yonse pamodzi inali mizinda 13 ndi midzi yawo.
7 Panalinso mizinda inayi iyi: Aini, Rimoni, Eteri ndi Asani pamodzi
ndi midzi yawo. 8 Dzikolo linaphatikizanso midzi yonse yozungulira
mizinda imeneyi mpaka ku Baalati-Beeri, ndiye kuti Rama wa kummwera.

Ili ndi dziko limene mabanja a fuko la Simeoni analandira kukhala lawo.
9 Cholowa cha fuko la Simeoni chinatengedwa kuchokera ku gawo la Yuda
chifukwa fuko la Yuda linali lalikulu kwambiri. Izi zinachititsa fuko la
Simeoni kukhala m'kati mwenimweni mwa dziko la Yuda.

*Dziko la Zebuloni*

10 Maere achitatu anagwera mabanja a fuko la Zebuloni:
Malire a dziko lawo anafika mpaka ku Saridi. 11 Malirewo anakwera
kupita cha kumadzulo ku Marala nakafika ku Dabeseti ndi ku mtsinje
wa kummawa kwa Yokineamu. 12 Kuchokera ku mbali ina ya Saridi
malire anakhota kupita kummawa ku malire a Kisiloti-Tabori mpaka
ku Daberati nakwera mpaka ku Yafiya. 13 Kuchokera kumeneko
anabzola kulowa cha kummawa mpaka ku Gati-Heferi ndi ku Eti Kazini
ndi kumaloza ku Neya njira ya ku Rimoni. 14 Mbali ya kumpoto
malirewo analoza ku Hanatoni ndipo anakathera ku chigwa cha Ifita

Eli. 15 Anaphatikizapo Katati, Nahalala, Simironi, Idala ndi Betelehemu.
Mizinda yonse inakwana khumi ndi iwiri pamodzi ndi midzi yake.
16 Mizinda imeneyi pamodzi ndi midzi yake ndi imene mabanja a fuko la
Zebuloni analandira.

### *Dziko la Isakara*

17 Maere achinayi anagwera mabanja a fuko la Isakara. 18 Dziko lawo
linaphatikiza zigawo izi:

Yezireeli, Kesuloti, Sunemu, 19 Hafaraimu, Sioni, Anaharati, 20 Rabiti,
Kisoni, Ebezi, 21 Remeti, Eni Ganimu, Eni Hada ndi Beti-Pazezi.
22 Malirewa anakafikanso ku Tabori, Sahazuma ndi Beti-Semesi ndipo
anakathera ku Yorodani. Mizinda yonse inalipo 16 ndi midzi yake.

23 Mizinda imeneyi pamodzi ndi midzi yake ndiyo inali cholowa cha
mabanja a fuko la Isakara.

### *Dziko la Aseri*

24 Maere achisanu anagwera mabanja a fuko la Aseri. 25 Gawo lawo
linaphatikiza

Helikati, Hali, Beteni, Akisafu, 26 Alameleki, Amadi ndi Misali.
Kumadzulo malire anafika ku Karimeli ndi Sihori Libinati. 27 Kenaka
anakhotera kummawa kulowera ku Beti-Dagoni nafika ku dziko la Ze-
buloni ndi ku chigwa cha Ifita Eli, ndipo anapita kumpoto ku Beti-Emeki
ndi Neieli. Anapitirirabe kumpoto mpaka kukafika ku Kabuli, 28 Ebroni,
Rehobu, Hamoni, ndi Kana, mpaka ku Sidoni Wamkulu. 29 Kenaka
malirewo anakhotera ku Rama ndi kupita ku mzinda wotetezedwa wa
ku Turo. Kuchokera pamenepo malirewo anakhota kupita ku Hosa
nakatulukira ku Nyanja, m'chigawo cha Akizibu, 30 Uma, Afeki ndi
Rehobu. Mizinda yonse inalipo 22 pamodzi ndi midzi yake.

31 Mizinda yonseyi pamodzi ndi midzi yake ndiyo inali cholowa cha
mabanja a fuko la Aseri.

### *Dziko la Nafutali*

32 Maere achisanu ndi chimodzi anagwera mabanja a fuko la Nafutali.

33 Malire awo anayambira ku Helefu mpaka ku mtengo wa thundu
wa ku Zaananimu, ndipo anapitirira n'kukafika ku Adami Nekebu,
Yabineeli mpaka ku Lakumi ndi kukathera ku Yorodani. 34 Tsono
malirewo anakhotera kumadzulo kupita ku Azinoti-Tabori. Kuchoka
kumeneko anapita ku Hukoki, modutsa Zebuloni cha kummwera, Aseri
cha kumadzulo ndi mtsinje wa Yorodani cha kummawa. 35 Mizinda
yotetezedwa inali Zidimi, Zeri, Hamati, Rakati, Kinereti, 36 Adama, Rama,
Hazori, 37 Kedesi, Ederi, Eni Hazori, 38 Yironi, Migidali Eli, Horemu, Beti-
Anati ndi Beti-Semesi. Yonse pamodzi inalipo mizinda 19 ndi midzi yake.

39 Mizinda yonseyi pamodzi ndi midzi yawo ndiyo inali cholowa cha
mabanja a fuko la Nafutali.

### *Dziko la Dani*

40 Maere achisanu ndi chiwiri anagwera mabanja a fuko la Dani. 41 Gawo
lawo linaphatikiza mizinda iyi:

Zora, Esitaoli, Iri Semesi, 42 Saalabini, Ayaloni, Itira, 43 Eloni, Timna,
Ekroni, 44 Eliteke, Gibetoni, Baalati, 45 Yehudi, Beni Beraki, Gati-Rimoni,
46 Me-Yarikoni ndi Rakoni, pamodzi ndi dera loyang'anana ndi Yopa.

47 Anthu a fuko la Dani atalandidwa dziko lawo, anapita kukathira
nkhondo Lesemu. Iwo anapha anthu ake onse, nawulandiratu mzindawo,

kuwusandutsa wawo ndi kumakhalamo. Tsono anatcha mzindawo dzina
loti Dani popeza ndilo linali dzina la kholo lawo.
48 Mizinda yonseyi pamodzi ndi midzi yake ndiyo inali cholowa cha
mabanja a fuko la Dani.

### *Dziko la Yoswa*

49 Atatha kugawana zigawo zosiyanasiyana za dzikolo, Aisraeli anamu-
patsa Yoswa mwana wa Nuni chigawo chake. 50 Potsata zimene Yehova
anawalamula, anamupatsa mzinda wa Timnati-Sera umene anawupem-
pha. Mzindawu unali m'dziko lamapiri la Efereimu. Iye anawumanga
mzindawu ndi kukhazikikako.
51 Wansembe Eliezara, Yoswa ndi atsogoleri a mabanja onse a Israeli
anagawa dziko lija zigawozigawo pogwiritsa ntchito maere pamaso pa
Yehova. Izi zinachitika ku Silo pa khomo la tenti ya msonkhano. Choncho
anamaliza kugawa dzikolo.

## 20

### *Mizinda Yopulumukiramo*

1 Pambuyo pake Yehova anati kwa Yoswa: 2 "Uza Aisraeli kuti apatule
mizinda yopulumukiramo, monga ine ndinakulangizira kudzera mwa
Mose, 3 kuti aliyense amene wapha munthu mosazindikira osati mwadala
azithawirako. Motero adzatetezedwa kwa wolipsira. 4 Ngati munthu
wathawira ku umodzi mwa mizinda imeneyi, akafike pa malo oweruzira
milandu amene ali pa chipata cha mzindawo ndipo akafotokoze mlandu
wake pamaso pa akuluakulu a mzindawo. Kenaka iwo adzamulola
kulowa mu mzinda wawo ndi kumupatsa malo woti akhale nawo. 5 Ngati
munthu wolipsirayo amutsatira komweko atsogoleriwo asapereke munthu
wakuphayo chifukwa anapha Mwisraeli mnzakeyo mosazindikira, osati
mwachiwembu. 6 Munthu wakuphayo adzakhalabe mu mzindawo mpaka
atayimbidwa mlandu pamaso pa gulu lonse, ndiponso mpaka atamwalira
mkulu wa ansembe amene akutumikira pa nthawiyo. Pamenepo
munthuyo atha kubwereranso ku mudzi kwawo kumene anachoka
mothawa kuja."
7 Choncho iwo anapatula Kedesi m'dera la Galileya ku mapiri a Nafutali,
Sekemu ku mapiri a Efereimu, ndi Kiriati Ariba (ndiye Hebroni) ku mapiri
a Yuda. 8 Kummawa kwa Yorodani, m'mapiri a chipululu a kummawa kwa
Yeriko, anapatula Bezeri pakati pa dera la fuko la Rubeni. Anapatulanso
Ramoti ku Giliyadi m'dera la fuko la Gadi, ndiponso Golani ku Basani
m'dera la fuko la Manase. 9 Imeneyi ndiyo inali mizinda yopulumukiramo
ya Aisraeli onse ngakhalenso mlendo wokhala pakati pawo. Munthu
aliyense wopha mnzake mwangozi ankathawira ku mizinda imeneyi.
Munthu wolipsira sankaloledwa kuti aphe munthu wothawayo ngati
mlandu wake sunazengedwe pamaso pa gulu lonse.

## 21

### *Mizinda ya Alevi*

1 Tsono atsogoleri a mabanja a fuko la Levi anabwera kwa wansembe
Eliezara, Yoswa mwana wa Nuni, ndi kwa atsogoleri a mabanja a mafuko
onse a Aisraeli, 2 ku Silo m'dziko la Kanaani ndipo anati, "Yehova
analamula kudzera mwa Mose kuti atipatse mizinda kuti tikhalemo,
pamodzi ndi malo odyetseramo ziweto zathu." 3 Choncho, Aisraeli

anapereka kwa fuko la Levi mizinda iyi pamodzi ndi malo owetera ziweto zawo kuchokera ku madera awo, monga Yehova analamulira:

[4] Maere oyamba anagwera mabanja a Kohati, Alevi amene anali zidzukulu za wansembe Aaroni anapatsidwa mizinda 13 kuchokera ku
mafuko a Yuda, Simeoni ndi Benjamini. [5] Ndipo mabanja otsala a Kohati
anapatsidwa mizinda khumi kuchokera ku mafuko a Efereimu, Dani ndi theka la fuko la Manase.

[6] Zidzukulu za Geresoni zinapatsidwa mizinda 13 kuchokera ku mabanja a mafuko a Isakara, Aseri, Nafutali ndi theka la fuko la Manase ku Basani.

[7] Mabanja a Merari anapatsidwa mizinda khumi ndi iwiri kuchokera ku mafuko a Rubeni, Gadi ndi Zebuloni.

[8] Choncho Aisraeli anapereka kwa fuko la Levi mizindayi pamodzi ndi malo odyetserako ziweto pogwiritsa ntchito maere, monga Yehova analamula kudzera mwa Mose.
[9] Awa ndi mayina a mizinda ya mafuko a Yuda ndi Simeoni imene
inaperekedwa kwa zidzukulu za Aaroni, [10] ku banja la Kohati amene
anali Alevi. Paja maere oyamba anagwera mabanja a Kohati kuti alandira mizinda.

[11] Anapatsidwa mzinda wa Kiriati Ariba. (Paja Ariba ndiye kholo la Anaaki). Dzina lina la mzindawu ndi Hebroni, ndipo unali m'dziko la mapiri la Yuda. Pamodzi ndi mzindawu anapatsidwanso mabusa ake
onse ozungulira. [12] Komabe minda ndi midzi yozungulira mizindayi inali itaperekedwa kale kwa Kalebe, mwana wa Yefune kuti ikhale cholowa chake.

[13] Choncho zidzukulu za Aaroni wansembe, zinapatsidwa Hebroni
(mzinda wopulumukirako amene wapha munthu), Libina, [14] Yatiri,
Esitemowa, [15] Holoni, Debri, [16] Aini, Yuta, ndi Beti-Semesi pamodzi ndi mabusa odyetseramo ziweto ozungulira mizindayi. Yonse pamodzi inali mizinda isanu ndi inayi yochokera ku mafuko awiriwa.

[17] Fuko la Benjamini linapereka Gibiyoni, Geba, [18] Anatoti ndi Alimoni,
pamodzi ndi mabusa odyetsera ziweto ozungulira mizindayi. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.
[19] Choncho mizinda 13 pamodzi ndi malo odyetsera ziweto anapatsidwa kwa ansembe, zidzukulu za Aaroni.
[20] Mabanja ena otsalira a Kohati a fuko la Levi anapatsidwa mizinda iyi kuchokera ku fuko la Efereimu:

[21] Mizinda ya Sekemu ndi Gezeri ndiye inali mizinda wopulumukirako munthu aliyense wopha mnzake mwangozi. Mizindayi inali ku mapiri
a Efereimu. [22] Analandiranso mizinda ya Gezeri, Kibuzaimu, Beti-Horoni pamodzi ndi malo odyetsera ziweto ozungulira mizindayi. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.

[23] Fuko la Dani linapereka mizinda ya Eliteke, Gibetoni, [24] Ayaloni,
Gati-Rimoni pamodzi ndi mabusa odyetsera ziweto ozungulira mizindayi. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.

[25] Kuchokera ku theka la fuko la Manase analandira Taanaki ndi Gati-Rimoni pamodzi ndi malo awo owetera ziweto, mizinda iwiri.
[26] Mizinda khumi yonseyi pamodzi ndi malo odyetsera ziweto, zinapatsidwa ku mabanja ena onse a Akohati.
[27] Mabanja a Ageresoni a fuko la Levi anapatsidwa mizinda iwiri
kuchokera ku theka la Manase wa kummawa,

Golani ku Basani (mzinda wopulumukirako amene wapha munthu mwangozi) ndi Beesitera, pamodzi ndi malo awo odyetserako ziweto.

28 Fuko la Isakara linapereka mizinda ya
Kisoni, Daberati, 29 Yarimuti ndi Eni Ganimu, pamodzi ndi malo awo odyetsera ziweto. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.

30 Fuko la Aseri linapereka mizinda ya
Misali, Abidoni, 31 Helikati ndi Rehobu pamodzi ndi malo awo odyetsera ziweto. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.

32 Fuko la Nafutali linapereka mizinda ya
Kedesi wa ku Galileya, mzinda umene unali wopulumukiramo munthu wopha mnzake mwangozi. Analandiranso mizinda ya Hamoti-Dori ndi Karitani. Kuphatikizira apa, analandira malo odyetsera ziweto a mizindayi. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.

33 Mabanja onse a Ageresoni analandira mizinda 13 pamodzi ndi malo awo odyetsera a ziweto.

34 Mabanja a Merari amene anali otsala a fuko la Levi, anapatsidwa
mizinda iyi kuchokera ku fuko la Zebuloni:
Yokineamu, Karita, 35 Dimuna ndi Nahalali, pamodzi ndi malo awo odyetsera ziweto. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.

36 Kuchokera ku fuko la Rubeni analandira
Bezeri, Yahaza, 37 Kedemoti ndi Mefaati, pamodzi ndi malo awo odyetsera ziweto. Yonse pamodzi inali mizinda inayi.

38 Kuchokera ku fuko la Gadi
analandira mzinda wa Ramoti ku Giliyadi. Mzinda umene unali wopulumukiramo munthu wopha mnzake mwangozi.
39 Analandiranso mizinda ya Mahanaimu, Hesiboni, Yazeri pamodzi ndi malo odyetserako ziweto ozungulira mizinda yonseyi. Yonse pamodzi inali mizindayi anayi.

40 Choncho mabanja onse a Merari, amene anali otsala a fuko la Levi analandira mizinda khumi ndi iwiri pogwiritsa ntchito maere.

41 Motero mizinda 48 ya m'dziko limene Aisraeli analanda inapatsidwa
kwa Alevi, kuphatikizapo malo ake odyetsera ziweto. 42 Iliyonse mwa
mizindayi inali ndi malo owetera ziweto oyizungulira.

43 Motero Yehova anapereka kwa Israeli dziko limene analumbira
kulipereka kwa makolo awo. Atalilandira anadzakhalamo. 44 Yehova
anawapatsa mtendere m'dziko lonse monga momwe analonjezera makolo awo. Palibe ndi mmodzi yemwe mwa adani awo amene anatha kuwagonjetsa chifukwa Yehova anapereka adani awo onse m'manja mwawo.
45 Yehova anakwaniritsa zonse zimene analonjeza kwa Aisraeli.

# 22

*Mafuko a Kummawa Abwerera Kwawo*

1 Pambuyo pake Yoswa anayitanitsa fuko la Rubeni, fuko la Gadi ndi
theka la fuko la Manase, 2 ndipo anawawuza kuti, "Inu mwachita zonse
zimene Mose mtumiki wa Yehova anakulamulani, ndipo mwamvera mu
zonse zimene ndinakulamulirani. 3 Aisraeli anzanu simunawasiye nthawi
yayitali yonseyi mpaka lero lino. Inu mwaonetsetsa kuti mwachita
zonse zimene Yehova anakulamulani. 4 Tsono pakuti Yehova Mulungu
wanu wapereka mpumulo kwa abale anu monga anayankhulira nawo,

bwererani ku nyumba zanu ku dziko limene Mose mtumiki wa Yehova
anakupatsani, dziko limene lili pa tsidya la Yorodani kummawa. 5 Koma
samalitsani kuti mumvere malamulo ndi malangizo amene Mose mtumiki
wa Yehova anakupatsani: kukonda Yehova Mulungu wanu, kuchita
zimene iye amafuna, kumvera malamulo ake, kukhala okhulupirika kwa
Iye ndi kumutumikira ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse.”

6 Ndipo Yoswa anawadalitsa ndi kuwalola kuti apite ndipo anapitadi ku
nyumba zawo. 7 Apa n’kuti Mose atapereka dziko la Basani ku theka lina la
fuko la Manase. Koma theka lina la fuko la Manase Yoswa analipatsa dziko
la kumadzulo kwa Yorodani pamodzi ndi abale awo onse. Pamene Yoswa
ankawatumiza kwawo anthu amenewa, anawadalitsa, 8 nawawuza kuti,
“Mukubwerera kwanu ndi chuma chambiri. Muli ndi ng’ombe zambiri
pamodzi ndi siliva, golide, mkuwa ndi chitsulo, ndiponso zovala zambiri.
Izi zimene munafunkha kwa adani anu agawireni abale anu.”

9 Choncho mafuko a Rubeni, Gadi, pamodzi ndi theka la fuko la Manase
anabwerera kwawo. Aisraeli ena onse anawasiya ku Silo m’dziko la
Kanaani. Tsono anapita ku dziko la Giliyadi, dziko limene linali lawo
popeza analilandira potsata malamulo a Yehova kudzera mwa Mose.

10 Atafika ku Geliloti, malo amene ali m’mbali mwa mtsinje wa Yorodani
m’dziko la Kanaani, fuko la Rubeni, fuko la Gadi ndi theka la fuko la
Manase anamanga guwa lansembe lalikulu pamenepo. 11 Ndipo pamene
Aisraeli ena onse anawuzidwa kuti anthu a fuko la Rubeni, fuko la Gadi
ndi theka la fuko la Manase amanga guwa lansembe m’malire a Kanaani
ku Geliloti, ku tsidya lathu lino la Yorodani, 12 gulu lonse la Aisraeli
linasonkhana ku Silo kuti lipite kukachita nawo nkhondo.

13 Choncho Aisraeli anatumiza Finehasi mwana wa wansembe, Eliezara
ku dziko la Giliyadi kwa mafuko a Rubeni, Gadi ndi theka la fuko
la Manase. 14 Pamodzi ndi Finehasiyo anatumiza akuluakulu khumi
ochokera ku fuko lililonse la Aisraeli. Aliyense mwa akuluakulu amenewa
anali mtsogoleri wa banja limodzi la mafuko a Aisraeli.

15 Atafika ku Giliyadi anawuza fuko la Rubeni, Gadi ndi theka lija la
fuko la Manase kuti, 16 “Gulu lonse likukufunsa kuti, ‘Chifukwa chiyani
mwachita chinthu chonyansa chotere potsutsana ndi Mulungu wa Israeli?
N’chifukwa chiyani mwapatuka ndi kuleka kutsata Yehova podzimangira
nokha guwa lansembe? Mwapandukiratu Yehova! 17 Kodi tchimo lija la
ku Peori ndi lochepa kwa inu? Paja Yehova analanga gulu lonse ndi mliri
chifukwa cha tchimolo, ndipo mpaka lero tchimo limene lija tikanazunzika
nalobe. 18 Kodi inu tsono mufuna kupatuka kuleka kumutsata Yehova?

“ ‘Ngati lero mumupandukira Yehovayo, ndiye kuti mawamawali Iye
adzakwiyira gulu lonse wa Israeli. 19 Ngati dziko limene inu mwatenga
ndi loyipitsidwa, bwerani ku dziko la Yehova kumene kuli chihema chake
kuja, ndipo mukhale nafe limodzi. Koma inu musawukire Yehova kapena
kutisandutsa ife kukhala opanduka podzimangira guwa lansembe, ku-
wonjezera pa guwa lansembe la Yehova Mulungu wanu. 20 Kumbukirani
pamene Akani mwana wa Zera anakana kumvera lamulo la zinthu
zoyenera kuwonongedwa, kodi suja mkwiyo wa Yehova unagwera gulu
lonse la Israeli? Akaniyo sanafe yekha chifukwa cha tchimo lakelo.’ ”

21 Tsono mafuko a Rubeni, Gadi ndi theka la fuko la Manase an-
awayankha atsogoleri a mabanja a Israeli aja kuti, 22 “Wamphamvu
uja, Mulungu ndiye Yehova! Wamphamvu uja Mulungu ndiye Yehova.
Iyeyu ndiye akudziwa chifukwa chiyani tinachita zimenezi. Tikufunanso

kuti inu mudziwe. Ngati tinachita izi mopandukira ndiponso moonetsa
kusakhulupirira Yehova, lero lomwe lino musatisiye ndi moyo. 23 Ngati
tinapandukira Yehova ndi kuleka kumutsata pamene tinadzimangira
guwa loti tizipserezerapo nsembe kapena kupereka nsembe zaufa, kapena
nsembe za mtendere, Yehova yekha ndiye atilange.

24 "Ayi! Ife tinachita izi kuopa kuti tsiku lina zidzukulu zanu zin-
gadzanene kwa zidzukulu zathu kuti, 'Kodi inu mukufuna chiyani kwa
Yehova Mulungu wa Israeli? 25 Yehova anayika mtsinje wa Yorodani
kukhala malire pakati pa ife ndi inu, anthu a fuko la Rubeni ndi Gadi.
Inuyo mulibe gawo mwa Yehova.' Tsono mwina zidzukulu zanuzo
n'kudzaletsa zathu kupembedza Yehova.

26 "N'chifukwa chake tinaganiza kuti, 'Tiyeni timange guwa lansembe,
koma osati kuti tiziperekapo nsembe zopsereza kapena zopereka.' 27 Koma
mosiyana ndi zimenezi, guwali likhale umboni pakati pa ife ndi inu
ndiponso mibado imene ikubwerayo, kuti ife timapembedzanso Yehova
ndi nsembe zathu zopsereza, zopereka, ndiponso nsembe za mtendere.
Motero m'tsogolo muno zidzukulu zanu sizidzatha kunena kwa zidzukulu
zathu kuti, 'Inu mulibe gawo mwa Yehova!'

28 "Ndipo ife tinati kuti, 'Ngati iwo adzatiyankhulira kapena
kuyankhulira zidzukulu zathu motero m'tsogolo muno, ife tidzayankha
kuti, onani guwa lansembe, lofanana ndi lomwe makolo athu anamanga
osati loperekerapo nsembe zopsereza kapena nsembe zina koma ngati
umboni pakati pa inu ndi ife.'

29 "Sizingatheke konse kuti ife lero n'kupandukira Yehova. Ife sitin-
gapatuke kuleka kumutsata Yehova ndi kumanga guwa lina la nsembe
zopsereza, nsembe za zakudya, ndi nsembe zina zopikisana ndi guwa la
Yehova, Mulungu wathu limene lili patsogolo pa Hema ya Yehova m'mene
amakhalamo."

30 Tsono Finehasi wansembe ndi atsogoleri a gululo amene anali naye
atamva zimene anthu a fuko la Rubeni, Gadi ndi theka lakummawa la
fuko la Manase ananena, anakondwera kwambiri. 31 Ndipo Finehasi
wansembe, mwana wa Eliezara anati kwa mafuko a Rubeni, Gadi ndi
Manase, "Lero tadziwa kuti Yehova ali nafe chifukwa zimene mwachitazi
simunawukire nazo Yehova. Inu mwapulumutsa Aisraeli onse ku chilango
cha Yehova."

32 Ndipo Finehasi mwana wa wansembe Eliezara, pamodzi ndi atso-
goleriwo anachoka ku Giliyadi nasiya anthu a fuko la Rubeni ndi Gadi
nabwerera ku Kanaani kwa Aisraeli anzawo, ndipo anakafotokoza zon-
sezi. 33 Mawu amenewa anakondweretsa Aisraeli onse ndipo anayamika
Mulungu. Choncho sanakambenso zopita ku nkhondo kukawononga dziko
limene Arubeni ndi Agadi ankakhalamo.

34 Arubeni ndi Agadi anatcha guwalo kuti Mboni: Mboni pakati pathu
kuti Yehova ndi Mulungu.

## 23

*Kutsanzika kwa Yoswa*

1 Panapita nthawi yayitali kuchokera pamene Yehova anakhazikitsa
mtendere pakati pa Aisraeli ndi adani awo owazungulira. Nthawi imeneyi
n'kuti Yoswa atakalamba, ali ndi zaka zambiri. 2 Yoswayo anayitanitsa Ais-
raeli onse pamodzi ndi akuluakulu, atsogoleri, oweruza, ndi oyang'anira
anthu antchito ndipo anawawuza kuti, "Ine ndakalamba ndipo ndili

ndi zaka zambiri. 3 Inu mwaona zonse zimene Yehova Mulungu wanu
wachita kwa mitundu yonseyi chifukwa cha inu. Ndi Yehova Mulungu
wanu amene anakumenyerani nkhondo. 4 Tsono onani! Mitundu ya
anthu otsalawa ndayipereka kwa mafuko anu pamodzi ndi mitundu ya
anthu ya pakati pa Yorodani ndi Nyanja Yayikulu ya kumadzulo imene
ndinayigonjetsa. 5 Yehova Mulungu wanu ndiye adzawathamangitsa
pamaso panu. Mudzatenga dziko lawo monga Yehova anakulonjezerani.

6 "Choncho khalani amphamvu, ndipo samalani kuti mumvere zonse
zimene zalembedwa m'buku la malamulo a Mose. Musapatuke pa
malamulo onse amene alembedwamo. 7 Musagwirizane ndi mitundu
ya anthu imene yatsala pakati panu. Musatchule mayina a milungu
yawo kapena kuyitchula polumbira. Musayitumikire kapena kuyigwadira.
8 Koma mukuyenera kugwiritsa Yehova Mulungu wanu, monga mwachi-
tira mpaka lero lino.

9 "Yehova wapirikitsa patsogolo panu mitundu ya anthu ikuluikulu ndi
yolimba. Mpaka lero palibe amene watha kulimbana nanu. 10 Aliyense
wa inu atha kuthamangitsa anthu 1,000 chifukwa Yehova Mulungu
wanu ndiye amakumenyerani nkhondo, monga momwe analonjezera.
11 Choncho samalitsani kuti mukonde Yehova Mulungu wanu.

12 "Koma ngati mubwerera m'mbuyo ndi kuphatikizana ndi mitundu
yotsalayi imene ili pakati panu ndi kumakwatirana nayo, 13 pamenepo
mudziwe kuti Yehova, Mulungu wanu, sadzapirikitsa mitundu imeneyi
pamaso panu, koma idzakhala ngati msampha kwa inu kapenanso
khwekhwe lokukolani. Idzakhala ngati zikwapu pa msana panu
kapenanso ngati minga m'maso mwanu mpaka mutatha psiti m'dziko
labwinoli limene Yehova Mulungu wanu wakupatsani.

14 "Aliyense wa inu akudziwa mu mtima mwake komanso m'moyo
mwake kuti zabwino zonse zimene Yehova Mulungu wanu anakulonjezani
zachitika. Palibe lonjezo ndi limodzi lomwe limene silinakwaniritsidwe.
15 Monga momwe Yehova Mulungu wanu wakuchitirani zabwino zonse
zimene ananena kuti adzachita, Yehovayo angathenso kukuchitirani
zoyipa zonse zimene waopseza, mpaka kukuchotsani m'dziko lokoma
limene anakupatsani. 16 Ngati muphwanya pangano la Yehova Mulungu
wanu, limene anakulamulirani n'kumapita kukatumikira milungu ina ndi
kuyigwadira, Yehova adzakukwiyirani, ndiye mudzachotsedwa m'dziko
labwinoli limene Yehova wakupatsani."

# 24

*Kukonzanso Pangano ku Sekemu*

1 Tsono Yoswa anasonkhanitsa mafuko onse a Israeli ku Sekemu. Iye
anayitanitsa akuluakulu, atsogoleri, oweruza, ndi akuluakulu a boma la
Israeli, ndipo iwo anafika pamaso pa Mulungu.

2 Yoswa anati kwa anthu onse, "Yehova Mulungu wa Israeli akuti,
'Kalekale makolo anu, kuphatikiza Tera, abambo a Abrahamu ndi Nahori
ankakhala kutsidya kwa Mtsinje ndipo ankapembedza milungu ina.
3 Koma ine ndinatenga kholo lanu Abrahamu kumuchotsa ku dziko la
kutsidya kwa mtsinje wa Yufurate ndipo ndinamutsogolera kupita ku
dziko la Kanaani. Ndinamupatsa zidzukulu zambiri. Ndinamupatsa Isake,
4 ndipo Isake ndinamupatsa Yakobo ndi Esau. Ndinapereka dziko la mapiri
la Seiri kwa Esau, koma Yakobo ndi ana ake anapita ku Igupto.

[5] " 'Kenaka ndinatuma Mose ndi Aaroni, ndipo ine ndinazunza Aigupto.
Pambuyo pake ndinakutulutsani. [6] Nditatulutsa makolo anu ku Igupto nd-
inafika nawo ku Nyanja Yofiira. Aigupto anawathamangira ndi magaleta
ndi okwera pa akavalo mpaka ku Nyanja Yofiira. [7] Tsono makolo anuwo
anapemphera kwa Ine kuti ndiwathandize, ndipo ndinayika mtambo
wakuda pakati pawo ndi Aiguptowo, ndipo Nyanja inamiza Aigupto aja.
Inu munaona ndi maso anu zimene ndinachita kwa Aiguptowo ndipo inu
munakhala m'chipululu nthawi yayitali.

[8] " 'Pambuyo pake Ine ndinabwera nanu ku dziko la Aamori amene
amakhala kummawa kwa Yorodani. Iwo anamenyana nanu koma
ndinawapereka m'dzanja lanu. Ndinawawononga pamaso panu, ndipo
inu munalanda dziko lawo. [9] Balaki mwana wa Zipori, mfumu ya
Mowabu, analimbana ndi Israeli. Iye anayitanitsa Balaamu mwana wa
Beori kuti akutemberereni. [10] Koma ine sindinamvere Balaamu, kotero
iye anakudalitsani mowirikiza ndipo ndinakulanditsani m'dzanja lake.

[11] " 'Ndipo inu munawoloka Yorodani ndi kufika ku Yeriko. Anthu a ku
Yeriko analimbana nanu pamodzi ndi Aamori, Aperezi, Akanaani, Ahiti,
Agirigasi, Ahivi ndi Ayebusi. Koma Ine ndinawapereka m'dzanja lanu.
[12] Ine ndinatumiza mavu amene anapirikitsa mafumu awiri Aamori aja
pamaso panu. Inu simunachite izi ndi lupanga ndi uta wanu. [13] Motero
ndinakupatsani dziko limene simunalivutikire ndiponso mizinda imene
simunamange. Inu mukukhala m'menemo ndi kumadya zipatso za
m'munda wamphesa ndi kuthyola zipatso m'mitengo ya olivi zimene
simunadzale.'

[14] "Ndipo tsopano wopani Yehova ndi kumutumikira Iye mokhulupirika
ndi moona. Chotsani milungu imene makolo anu ankapembedza kutsidya
kwa mtsinje wa Yufurate ndi ku Igupto ndipo tumikirani Yehova. [15] Koma
ngati kutumikira Yehova kukuyipirani, sankhani lero amene mudzamu-
tumikire, kapena milungu imene makolo anu ankayitumikira kutsidya
kwa mtsinje wa Yufurate, kapena milungu ya Aamori, amene mukukhala
m'dziko lawo. Koma ine ndi banja langa, tidzatumikira Yehova."

[16] Ndipo anthu anayankha, "Sizingatheke kuti timusiye Yehova ndi
kutumikira milungu ina! [17] Yehova Mulungu wathu ndiye amene
anatitulutsa ife ndi makolo athu mu ukapolo, m'dziko la Igupto. Tinaona
ndi maso athu zizindikiro zozizwitsa zimene anachita. Iye anatiteteza pa
ulendo wathu wonse ndi pakati pa mitundu yonse imene tinkakumana
nayo. [18] Ife tikufika Iye anapirikitsa anthu onse pamodzi ndi Aamori
amene ankakhala m'dzikoli. Ifenso tidzatumikira Yehova chifukwa Iye
ndiye Mulungu."

[19] Koma Yoswa anati kwa anthuwo, "Inutu simungathe kutumikira
Yehova. Iye ndi Mulungu woyera, salola kupikisana naye. Sadzakukhu-
lulukirani ngati mumuwukira ndi kumuchimwira. [20] Ngati inu musiya
Yehova ndi kutumikira milungu yachilendo, adzakufulatirani. Iye adza-
kulangani ndi kukuwononganі ngakhale kuti poyamba anakuchitirani
zabwino."

[21] Koma anthuwo anati kwa Yoswa, "Ayi! Ife tidzatumikira Yehova."

[22] Kenaka Yoswa anati, "Inu mukudzichitira nokha umboni kuti
mwasankha kutumikira Yehova."

Iwo anayankha kuti, "Inde ife ndife mboni."

[23] Yoswa anati, "Tsono chotsani milungu yachilendo imene ili pakati
panu ndipo perekani mitima yanu kwa Yehova Mulungu wa Israeli."

24 Ndipo anthuwo anati kwa Yoswa, “Ife tidzatumikira Yehova Mulungu wathu ndi kumvera Iye.”

25 Choncho pa tsiku limenelo Yoswa anachita pangano m'malo mwa anthuwo, ndipo pa Sekemu pomwepo iye anapereka malamulo ndi
malangizo kwa anthu aja. 26 Ndipo Yoswa analemba zinthu izi m'buku la
malamulo a Mulungu. Kenaka iye anatenga mwala waukulu nawuyimika pansi pa mtengo wa thundu pa malo wopatulika a Yehova.

27 Yoswa anati kwa anthu onse, “Tamvani! Mwala uwu udzakhala mboni yotitsutsa. Mwalawu wamva mawu onse amene Yehova wayankhula kwa ife. Udzakhala mboni yotitsutsa ngati mukhala osakhulupirika kwa Mulungu wanu.”

*Kumwalira kwa Yoswa ndi Eliezara*

28 Kenaka Yoswa analola anthu kuti apite, aliyense ku dera lake.

29 Zitatha zinthu izi, Yoswa mwana wa Nuni, mtumiki wa Yehova,
anamwalira ali ndi zaka 110, 30 ndipo anamuyika m'manda m'dziko lake,
ku Timnati-Sera dziko lamapiri la ku Efereimu, kumpoto kwa phiri la Gaasi.

31 Israeli anatumikira Yehova pa nthawi yonse imene Yoswa anali ndi moyo ndiponso pa nthawi ya akuluakulu amene anali moyo Yoswa atamwalira, anthu amene ankadziwa zonse zimene Yehova anachitira Israeli.

32 Ndipo mafupa a Yosefe amene Aisraeli anawatulutsa ku Igupto anawayika m'manda a ku Sekemu pa malo amene Yakobo anagula ndi ndalama zasiliva 100 kwa ana a Hamori, abambo a Sekemu. Malo awa anakhala cholowa cha adzukulu a Yosefe.

33 Ndipo Eliezara mwana wa Aaroni anamwalira ndipo anayikidwa m'manda ku Gibeya, malo amene anapatsidwa kwa Finehasi mwana wake, m'dziko lamapiri la Efereimu.

# Oweruza

*Aisraeli Achita Nkhondo ndi Akanaani Otsala*

1 Atamwalira Yoswa Aisraeli anafunsa Yehova kuti, “Ndani mwa ife
ayambe nkhondo yomenyana ndi Akanaani?”

2 Yehova anayankha kuti, “Fuko la Yuda ndilo liyambe kupita. Ndawap-
atsa dzikolo m’manja mwawo.”

3 Choncho Ayuda anawuza abale awo a fuko la Simeoni kuti, “Bw-
erani tipitire limodzi m’dziko limene tapatsidwa kuti tikamenyane ndi
Akanaani. Ifenso tidzapita nanu m’dziko limene anakugawirani.” Ndipo
Asimeoni anapita nawo.

4 Choncho Ayuda ananyamuka, ndipo Yehova anapereka Akanaani
ndi Aperezi m’manja mwawo. Ndipo anapha anthu 10,000 ku Bezeki.
5 Ku Bezekiko anakumana ndi ankhondo a mfumu Adoni-Bezeki ndipo
anamenyana nawo, ndipo Ayudawo anagonjetsa Akanaani ndi Aperezi.
6 Adoni-Bezekiyo anathawa, koma anamuthamangira ndi kumupeza,
namugwira. Atamugwira anamudula zala zake zazikulu za ku manja ndi
miyendo.

7 Tsono Adoni-Bezeki anati, “Mafumu 70 omwe anadulidwa zala
zazikulu za ku manja ndi miyendo yawo ankatola nyenyeswa pansi pa
tebulo langa. Mulungu tsopano wandibwezera zomwe ndinawachita.”
Kenaka anapita naye ku Yerusalemu ndipo anafera komweko.

8 Pambuyo pake Ayuda anakathira nkhondo mzinda wa Yerusalemu
ndipo anawulanda. Anapha anthu ambiri ndi kutentha mzinda wonse.

9 Kenaka Ayuda anapita kukamenyana ndi Akanaani omwe amakhala
ku dziko la ku mapiri, dziko la Negevi kummwera ndiponso mu zigwa.
10 Anakalimbananso ndi Akanaani amene ankakhala ku Hebroni (mzinda
womwe kale unkatchedwa Kiriyati-Araba). Kumeneko anagonjetsa Sesai,
Ahimani ndi Talimai.

11 Kuchokera kumeneko, iwo anakathira nkhondo anthu amene
ankakhala ku Debri (mzindawu poyamba unkatchedwa Kiriati Seferi).
12 Tsono Kalebe anati, “Munthu amene angathire nkhondo mzinda wa
Kiriati Seferi ndi kuwulanda, ndidzamupatsa mwana wanga Akisa kuti
akhale mkazi wake.” 13 Otanieli mwana wa Kenazi, mng’ono wake wa
Kalebe, ndiye anawulanda. Choncho Kalebe anamupatsa mwana wake
Akisa kuti akhale mkazi wake.

14 Tsiku lina atafika Akisayo, Otanieli anamuwumiriza mkazi wakeyo
kuti apemphe munda kwa Kalebe abambo ake. Pamene Akisa anatsika pa
bulu wake, Kalebe anamufunsa kuti, “Kodi ukufuna ndikuchitire chiyani?”

15 Iye anayankha kuti, “Mundikomere mtima. Popeza mwandipatsa ku
Negevi, kumalo kumene kulibe madzi, mundipatsenso akasupe amadzi.”
Choncho Kalebe anamupatsa akasupe a kumtunda ndi a kumunsi.

16 Tsono zidzukulu za Hobabu, Mkeni uja, mpongozi wa Mose, zinachoka
ku Yeriko mzinda wa migwalangwa pamodzi ndi anthu a fuko la Yuda
mpaka ku chipululu chimene chili kummwera kwa Aradi ndi kukakhala
ndi Aamaleki.

17 Kenaka anthu a fuko la Yuda anapita pamodzi ndi abale awo a fuko
la Simeoni ndi kukagonjetsa Akanaani amene amakhala ku Zefati, ndipo
mzindawo anawuwononga kwambiri. Choncho mzindawo anawutcha

Horima. 18 Anthu a fuko la Yuda analandanso mzinda wa Gaza ndi dziko
lonse lozungulira, mzinda wa Asikeloni pamodzi ndi dziko lake lonse
lozungulira, ndi mzinda wa Ekroni pamodzi ndi dziko lonse lozungulira.
19 Yehova anathandiza anthu a fuko la Yuda. Iwo analanda dziko la
kumapiri, koma sanathe kuwachotsa anthu ku zigwa, chifukwa anali
ndi magaleta azitsulo. 20 Monga analonjezera Mose, Kalebe anapatsidwa
Hebroni. Kalebe anapirikitsa mafuko atatu a Anaki mu mzindamo.
21 Koma fuko la Benjamini linalephera kuwachotsa Ayebusi, amene
amakhala mu Yerusalemu. Choncho Ayebusiwo akukhalabe ndi fuko la
Benjamini mu Yerusalemu mpaka lero.
22 A banja la Yosefe nawonso anathira nkhondo mzinda wa Beteli,
ndipo Yehova anali nawo. 23 Anatumiza anthu kuti akazonde Beteli.
Mzindawo kale unkatchedwa Luzi. 24 Anthu okazondawo anaona munthu
akutuluka mu mzindamo ndipo anamuwuza kuti, "Tisonyeze njira yolow-
era mu mzindamu, ndipo ife tidzakuchitira chifundo." 25 Choncho iye
anawaonetsa njirayo, ndipo iwo anapha anthu onse mu mzindamo ndi
lupanga koma munthu uja pamodzi ndi banja lake sanawaphe. 26 Ndipo
iye anapita ku dziko la Ahiti, kumene anamangako mzinda nawutcha
dzina lake Luzi. Mpaka lero lino mzindawo dzina lake ndi lomwelo.
27 Koma a fuko la Manase sanachotse nzika za mzinda wa Beti-Seani
pamodzi ndi m'midzi yake yozungulira, kapena nzika za mzinda wa
Taanaki ndi m'midzi yake yozungulira, kapenanso nzika za mzinda
wa Dori ndi m'midzi yake yozungulira. Iwo sanapirikitse nzika za
mzinda wa Ibuleamu ndi m'midzi yake yozungulira, kapena mzinda wa
Megido ndi m'midzi yake yozungulira. Choncho Akanaani anapitirirabe
kukhala m'dzikomo. 28 Aisraeli atakhala amphamvu, anawagwiritsa
Akanaaniwo ntchito yakalavulagaga, koma sanawapirikitse. 29 Nawonso
Aefereimu sanathamangitse Akanaani amene amakhala mu Gezeri, chon-
cho Akanaaniwo ankakhalabe pakati pawo ku Gezeriko. 30 Azebuloni
sanathamangitse Akanaani amene amakhala mu Kitironi kapena a ku
Nahaloli. Iwo ankakhala pakati pawo ndipo ankawagwiritsa ntchito
yakalavulagaga. 31 A fuko la Aseri nawo sanathamangitse amene
amakhala mu Ako, Sidoni, Ahilabu, Akizibu, Heliba, Afiki, ndi Rehobu.
32 Choncho anthu a fuko la Aseri anakhala pakati pa Akanaani amene
ankakhala m'dzikomo popeza sanawapirikitse. 33 Nalonso fuko la Nafutali
silinathamangitse anthu amene ankakhala ku Beti Semesi kapena ku Beti
Anati. Koma Anafutaliwo ankakhala pakati pa Akanaaniwo m'dzikomo.
Koma anthu amene ankakhala ku Beti Semesi ndi ku Beti Anati anawasan-
dutsa kukhala ogwira ntchito yathangata. 34 Aamori anapirikitsira anthu
a fuko la Dani ku dziko la ku mapiri popeza sanawalole kuti atsikire
ku chigwa. 35 Aamori anatsimikiza mtima zokhalabe ku phiri la Hara-
Heresi, ku Ayaloni, ndiponso ku Saalibimu. Koma a fuko la Yosefe anakula
mphamvu ndipo anagwiritsa Aamoriwo ntchito yakalavulagaga. 36 Malire
a Aamori anayambira ku chikweza cha Akirabimu n'kulowera ku Sela
napitirira kumapita chakumapiri ndithu.

# 2

*Mngelo wa Yehova ku Bokimu*

1 Mngelo wa Yehova anapita ku Bokimu kuchokera ku Giligala ndipo
anati kwa Aisraeli, "Ndinakutulutsani m'dziko la Igupto ndikukulowetsani
m'dziko limene ndinalumbira kwa makolo anu. Ndinati 'Sindidzaswa

pangano langa ndi inu, 2 ndipo inu musadzachite pangano ndi anthu
a dziko lino, koma mudzaphwanye maguwa awo ansembe.’ Koma
inu simunamvere lamulo langa. Chifukwa chiyani mwachita zimenezi?
3 Ndikukuwuzani tsopano kuti sindithamangitsa nzikazo pamene inu
mukufika. Ndidzawasandutsa kukhala adani anu ndipo milungu yawo
idzakhala ngati msampha kwa inu.”

4 Mngelo wa Mulungu atayankhula izi kwa Aisraeli, onse analira
mokweza, 5 ndipo anatcha malowo kuti Bokimu (kutanthauza kuti Olira).
Pamenepo anapereka nsembe kwa Yehova.

### *Agonjetsedwa Chifukwa Chosamvera*

6 Yoswa atawuza Aisraeli kuti achoke, iwo anapita kukatenga dzikolo,
aliyense dera lake. 7 Anthuwo anatumikira Yehova masiku onse a moyo
wa Yoswa. Atamwalira Yoswa, Aisraeli anatumikirabe Yehova nthawi
yonse ya moyo wa akuluakulu amene anaona zazikulu zimene Yehova
anawachitira.

8 Yoswa mwana wa Nuni, mtumiki wa Yehova, anamwalira ali ndi zaka
110. 9 Ndipo anamuyika m’manda a m’dziko lake, ku Timnati-Heresi
m’dziko la mapiri la Efereimu, kumpoto kwa phiri la Gaasi.

10 M’bado onse utapita kukakhala ndi anthu a mtundu awo, ke-
naka panauka m’bado wina umene sunadziwe Yehova ngakhale ntchito
zazikulu zimene Yehova anachitira Aisraeli. 11 Choncho Aisraeli anayamba
kuchita zinthu zoyipa pamaso pa Yehova ndipo anatumikira Abaala.
12 Iwo anasiya Yehova Mulungu wa makolo awo, amene anawatulutsa
ku Igupto. Ndipo anatsatira ndi kupembedza milungu yosiyanasiyana ya
anthu amene anawazungulira. Motero Aisraeli anakwiyitsa Yehova. 13 Iwo
anasiya Yehova ndi kumatumikira Baala ndi Asiteroti. 14 Yehova anapsera
mtima Aisraeli ndipo anawapereka m’manja mwa anthu ofunkha amene
ankasakaza zinthu zawo. Ndipo analola kuti adani awo owazungulira
amene sanathenso kulimbana nawo, awagonjetse. 15 Nthawi zonse
Aisraeli ankati akapita ku nkhondo, Yehova amalimbana nawo kuti
agonjetsedwe, monga ananenera molumbira kuti zidzaterodi. Choncho
iwo anali pa mavuto aakulu.

16 Choncho Yehova anawawutsira atsogoleri amene ankawapulumutsa
m’manja mwa anthu amene ankasakaza zinthu zawo. 17 Komabe iwo
sanawamvere atsogoleri awowo popeza ankapembedza milungu ina ndi
kumayigwadira. Iwo anapatuka msangamsanga mu njira imene ankayen-
damo makolo awo. Iwo aja ankamvera malamulo a Yehova, koma m’bado
uwu ayi. 18 Nthawi zonse Yehova akawautsira mtsogoleri, Iye amakhala
naye, ndipo mtsogoleriyo ankawapulumutsa Aisraeliwo m’manja mwa
adani awo m’nthawi imene anali moyo. Yehova ankawamvera chisoni Ais-
raeli pamene ankabuwula chifukwa cha anthu owazunza ndi kuwasautsa.
19 Koma nthawi zonse mtsogoleri akamwalira, Aisraeli ankabwerera
m’mbuyo. Iwo amadzisandutsa oyipa kupambana makolo awo popeza
ankatsata milungu ina, kuyitumikira ndi kumayigwadira. Anakana kusiya
makhalidwe awo oyipa ndi njira zawo zamakani.

20 Choncho Yehova anawapsera mtima Aisraeli ndipo anati, “Chifukwa
mtundu uwu waswa pangano limene ndinakhazikitsa ndi makolo awo
ndipo sanandimvere, 21 Inenso sindidzapirikitsanso mtundu uli wonse wa
anthu amene Yoswa anawasiya pomwalira. 22 Ndidzatero kuti ndiwayese
Aisraeli ndi kuona ngati adzasamala kuyenda m’njira ya Ine Yehova
monga momwe ankachitira makolo awo.” 23 Choncho Yehova anayileka

mitundu imeneyi ndipo sanayithamangitse kapena kuyipereka m'manja mwa Yoswa.

# 3

1 Iyi ndi mitundu ya anthu yomwe Yehova anayisiyiya kuti ayese nayo
Aisraeli amene sanadziwe kumenya nkhondo mu Kanaani 2 (Yehova
anachita izi kuti Aisraeli onse aphunzire kumenya nkhondo; makamaka
amene n'kale lonse sanadziwe kumenya nkhondo. 3 Mitundu ya anthuyo
ndi: Mafumu asanu a Afilisti, Akanaani onse, Asidoni, ndi Ahivi amene
ankakhala ku mapiri a Lebanoni kuyambira ku phiri la Baala-Herimoni
mpaka ku Lebo Hamati. 4 Iwowa Yehova anawasiya kuti aziyesa nawo
Aisraeli kuti aone ngati angamvere malamulo a Yehova, amene anapatsa
makolo awo kudzera mwa Mose.
5 Choncho Aisraeli anakhala pakati pa Akanaani, Ahiti, Aamori, Aperezi,
Ahivi ndi Ayebusi. 6 Tsono Aisraeli aja amalola ana awo aamuna ndi
aakazi kuti azikwatira ndi kukwatiwa ndi anthu amitundu ina. Kenaka
anayamba kupembedza milungu yawo.

### *Otanieli*

7 Aisraeli anachita zinthu zoyipira Yehova. Iwowa anayiwala Yehova
Mulungu wawo ndi kumatumikira Abaala ndi Asera. 8 Choncho Yehova
anawapsera mtima Aisraeliwo ndipo anawagulitsa kwa Kusani-Risataimu
mfumu ya ku Mesopotamiya. Choncho Aisraeli anakhala pansi pa
ulamuliro wake zaka zisanu ndi zitatu. 9 Koma pamene Aisraeliwo
analirira kwa Yehova, Iye anawawutsira mpulumutsi, Otanieli mwana
wamwamuna wa Kenazi, mng'ono wake wa Kalebe. Iyeyu ndiye
anawapulumutsa. 10 Mzimu wa Yehova unatsika pa iye, choncho anasan-
duka mtsogoleri wa Israeli. Iye anapita kukamenya nkhondo, ndipo
Yehova anapereka Kusani-Risataimu mfumu ya Aaramu m'manja mwake.
Choncho anayigonjetsa. 11 Ndipo m'dzikomo munakhala mtendere zaka
makumi anayi. Kenaka Otanieli mwana wa Kenazi anamwalira.

### *Ehudi*

12 Aisraeli anachitanso zinthu zoyipira Yehova. Tsono Yehova anapatsa
mphamvu Egiloni, mfumu ya Mowabu kuti alimbane ndi Aisraeli aja
popeza anachita zinthu zoyipira Yehova. 13 Egiloniyo anamemeza Aamori
ndi Aamaleki kupita kukamenyana ndi Israeli, ndipo analanda Yeriko,
mzinda wa migwalangwa. 14 Aisraeli anatumikira ngati akapolo Egiloni
mfumu ya Mowabu kwa zaka 18.
15 Aisraeli analiranso kwa Yehova, ndipo Iye anawawutsira mpulu-
mutsi, Ehudi. Iyeyu anali mwana wa Gera, munthu wamanzere, wa
fuko la Benjamini. Aisraeli ankatumiza msonkho kwa Egiloni, mfumu
ya Mowabu, kudzera kwa Ehudi. 16 Ndipo Ehudi anapanga lupanga
lakuthwa kuwiri lotalika masentimita makumi asanu, ndipo anamangirira
lupangalo pa ntchafu yake ya kumanja m'kati mwa zovala zake. 17 Iye
anakapereka msonkho kwa Egiloni, mfumu ya Mowabu, amene anali
munthu wonenepa kwambiri. 18 Ehudi atapereka msonkhowo, anawuza
anthu amene ananyamula msonkhowo kuti azipita. 19 Iye mwini anab-
werera pamalo a miyala yozokotedwa ku Giligala ndipo anati, "Zikomo
mfumu, ine ndili ndi mawu achinsinsi kuti ndikuwuzeni."
Mfumuyo inawuza onse amene amayitumikira kuti akhale chete, ndipo kenaka anawatulutsa.

[20] Kenaka Ehudi anayandikira pafupi ndi mfumuyo, ndipo iyo inakhala
yokha m'chipinda chapamwamba, mozizira bwino. Tsono Ehudi anati,
"Ndili ndi mawu ochokera kwa Mulungu woti ndikuuwuzeni." Mfu-
muyo itadzuka pa mpando wake waufumu, [21] Ehudi ndi dzanja lake
lamanzere, anasolola lupanga pa ntchafu yake ya kumanja ndi kubaya
nalo mfumuyo pa mimba. [22] Lupanga linalowa m'mimba pamodzi
ndi chogwirira chake. Mafuta anaphimba lupangalo popeza silinatulut-
sidwe m'mimbamo. Ndiponso matumbo anatuluka. [23] Kenaka Ehudi
anatuluka panja pa khonde, atatseka ndi kukhoma zitseko za chipinda
chapamwambacho.

[24] Ehudi atachoka, atumiki a mfumu aja anabwera, ndipo ataona kuti
zitseko za chipinda chapamwamba zinali zokhoma anaganiza kuti mwina
mfumu ikudzithandiza m'katimo. [25] Iwo anadikira nthawi yayitali koma
popanda chochitika. Koma ataona kuti mfumuyo sikutsekulabe zitseko
za chipindacho, iwo anatenga makiyi ndi kutsekula zitsekozo, ndipo
anangoona mbuye wawo atagwera pansi, ali wakufa.

[26] Ehudi anathawa pamene iwo ankadikira. Iye anadzera ku malo
a miyala yozokotedwa kuja ndi kuthawa kupita ku Seiri. [27] Atafika
kumeneko, anayimba lipenga ku dziko la ku mapiri la Efereimu. Iye
akutsogolera, Aisraeli onse anatsika naye pamodzi kuchoka ku mapiriko.

[28] Iye anawawuza kuti, "Nditsatireni, chifukwa Yehova wapereka
Amowabu, adani anu m'manja mwanu." Choncho anthuwo anamutsatira,
nalanda madooko a Yorodani opita ku Mowabu. Iwo sanalole kuti
wina aliyense awoloke. [29] Nthawi imeneyo anapha Amowabu pafupifupi
10,000. Ophedwawo anali anthu amphamvu komanso odziwa kumenya
nkhondo, ndipo panalibe ndi mmodzi yemwe anathawa. [30] Tsiku limenelo
Amowabu anakhala pansi pa ulamuliro wa Israeli, ndipo dzikolo linakhala
pa mtendere kwa zaka 80.

### *Samugara*

[31] Ehudi atamwalira, panabwera Samugara mwana wa Anati. Iye
anapha Afilisti 600 ndi ndodo yomenyera ng'ombe. Nayenso anapulu-
mutsa Israeli.

## 4

### *Debora*

[1] Ehudi atamwalira, Aisraeli anachitanso zinthu zoyipira Yehova.
[2] Choncho Yehova anawapereka m'manja mwa Yabini, mfumu ya ku
Kanaani, imene inkalamulira ku Hazori. Mkulu wa ankhondo ake anali
Sisera, amene ankakhala ku Haroseti-Hagoyimu. [3] Aisraeli analira kwa
Yehova kuti awathandize, chifukwa Sisera anali ndi magaleta achitsulo
900 ndipo anazunza Aisraeli mwankhanza kwa zaka makumi awiri.

[4] Debora, mneneri wamkazi, mkazi wake wa Rapidoti ndiye ankatso-
golera Israeli nthawi imeneyo. [5] Iye ankakhala pansi pa mtengo wa
mgwalangwa wa Debora, pakati pa Rama ndi Beteli m'dziko la ku mapiri
la Efereimu, ndipo Aisraeli ankapita kwa iye kuti akaweruze milandu
yawo. [6] Debora uja anatuma munthu kuti akayitane Baraki mwana wa
Abinoamu wa ku Kedesi m'dziko la Nafutali ndipo anati kwa iye, "Yehova
Mulungu wa Israeli akukulamula iwe kuti, 'Pita kasonkhanitse anthu ku
phiri la Tabori. Ubwere nawo anthu 10,000 a fuko la Nafutali ndi a fuko la
Zebuloni. [7] Ine ndidzakokera Sisera mkulu wa ankhondo a Yabini pamodzi

ndi magaleta ake ndi asilikali ake kwa inu ku mtsinje wa Kisoni ndipo
ndidzamupereka m'manja mwanu.' "

8 Baraki anamuyankha kuti, "Mukapita nane limodzi ine ndipita. Koma
ngati sitipitira limodzi, inenso sindipita."

9 Debora anati, "Chabwino, ine ndipita nawe limodzi. Koma mudziwe
kuti inu simudzalandirapo ulemu pa zimene mwachitazi popeza Yehova
wapereka Sisera m'manja mwa munthu wamkazi." Choncho Debora
ananyamuka kupita ku Kedesi pamodzi ndi Baraki. 10 Baraki anayitana
mafuko a Zebuloni ndi Nafutali kuti abwere ku Kedesi. Anthu 10,000
anamutsatira, ndipo Debora anapita naye pamodzi.

11 Nthawi imeneyo n'kuti Mkeni wina dzina lake Heberi atalekana ndi
Akeni anzake, zidzukulu za Hobabu, mlamu wa Mose, nakamanga tenti
yake pafupi ndi mtengo wa thundu ku Zananimu pafupi ndi Kedesi.

12 Pamene Sisera anamva kuti Baraki mwana wa Abinoamu wapita ku
phiri la Tabori, 13 anasonkhanitsa magaleta ake achitsulo 900 ndi anthu
onse amene anali naye ndipo anachoka ku Haroseti-Hagoyimu kupita ku
mtsinje wa Kisoni.

14 Debora anawuza Baraki kuti, "Dzukani! Paja ndi lero limene
Yehova wapereka Sisera m'manja mwako. Kodi Yehova sanakhale
akukutsogolerani?" Choncho Baraki anatsika phiri la Tabori, anthu 10,000
akumutsata. 15 Yehova anasokoneza Sisera ndi magaleta ake pamodzi ndi
ankhondo ake onse. Baraki ndi anthu ake anawapirikitsa ndipo Sisera
anatsika pa galeta yake nayamba kuthawa pansi. 16 Baraki analondola
magaletawo pamodzi ndi ankhondo onse mpaka ku Haroseti-Hagoyimu,
ndipo ankhondo onse a Sisera anaphedwa ndi lupanga. Palibe munthu
ndi mmodzi yemwe anatsala.

17 Komabe Sisera anathawa pansi mpaka anakafika ku tenti ya Yaeli
mkazi wa Heberi Mkeni uja, chifukwa panali mtendere pakati pa Yabini
mfumu ya Hazori ndi banja la Heberi, Mkeni uja.

18 Yaeli anatuluka kukachingamira Sisera ndipo anati, "Bwerani mbuye
wanga, lowani momwemo musaope." Choncho analowa m'tenti muja,
ndipo anamufunditsa chofunda.

19 Anati, "Ndili ndi ludzu, chonde patseniko madzi pang'ono akumwa,
ndili ndi ludzu." Mkaziyo anatsekula thumba la chikopa mmene munali
mkaka, namupatsa kuti amwe, ndipo anamufunditsanso.

20 Kenaka anawuza mkaziyo kuti, "Muyime pa khomo la tentili, ndipo
munthu wina akabwera kudzakufunsani kuti, 'Kodi kwafika munthu wina
kuno?' Inu muyankha kuti, 'Ayi.' "

21 Koma Yaeli mkazi wa Heberi, anatenga chikhomo cha tenti ndi
hamara ndi kupita mwakachetechete kwa Sisera uja. Tsono Sisera
ali mtulo chifukwa chotopa, mkazi uja anamukhomera chikhomo chija
m'mutu mwake. Chinatulukira kwinaku mpaka kulowa m'nthaka, ndipo
anafa pomwepo.

22 Baraki atafika akulondola Sisera, Yaeli anatuluka kukamuchingamira
namuwuza kuti, "Lowani mudzaone munthu amene mukumufunafuna."
Tsono atalowa anangoona Sisera ali thapsa pansi wakufa ndi chikhomo
chili m'mutu mwake.

23 "Choncho pa tsiku limenelo Mulungu anagonjetsa Yabini mfumu ya
Akanaani, pamaso pa Aisraeli. 24 Ndipo Aisraeli anapanikizabe Yabini,
mfumu ya Akanaani, mpaka kumuwonongeratu.

# 5

*Nyimbo ya Debora*

1 “Tsiku limenelo Debora ndi Baraki mwana wa Abinoamu anayimba
nyimbo iyi:

2 “Popeza kuti atsogoleri anatsogoleradi m’dziko la Israeli;
ndipo anthu anadzipereka okha mwa ufulu,
tamandani Yehova:

3 “Imvani inu mafumu! Tcherani khutu, atsogoleri inu!
Ndidzayimba nyimbo, ndidzayimbira Yehova,
Mulungu wa Israeli nyimbo yokoma.

4 “Inu Yehova, pamene munkatuluka mu Seiri,
pamene mumayenda kuchokera m’dziko la Edomu,
dziko linagwedezeka, mitambo inasungunuka
nigwetsa madzi.
5 Mapiri anagwedezeka pamaso pa Yehova,
Mulungu wa Israeli.

6 “Pa nthawi ya Samugara mwana wa Anati,
pa nthawi ya Yaeli, misewu inasiyidwa;
alendo ankangoyenda m’tinjira takumbali.
7 Anthu a ku midzi anathawa; mu Israeli munalibe midzi
mpaka pamene iwe Debora unafika;
unafika ngati mayi ku Israeli.
8 Pamene anasankha milungu ina,
nkhondo inabwera ku zipata za mzinda,
ndipo chishango kapena mkondo sizinapezeke
pakati pa anthu 40,000 mu Israeli.
9 Mtima wanga uli ndi atsogoleri a Israeli,
uli ndi anthu amene anadzipereka okha mwaufulu pakati pa anthu.
Tamandani Yehova!

10 “Inu okwera pa abulu oyera,
okhala pa zishalo,
ndi inu oyenda pa msewu,
yankhulani. 11 Ku zitsime, kutali ndi phokoso la a mauta;
kumeneko akusimba za kuti Yehova wapambana;
akusimba kuti Yehova walipsira anthu ake mu Israeli.

“Choncho anthu a Yehova
anasonkhana ku zipata za mzinda.
12 Anati, ‘Tsogolera ndiwe, Debora, tsogolera;
tsogolera ndiwe, tsogolera, imba nyimbo.
Iwe Baraki! nyamuka
Tsogolera akapolo ako, iwe mwana wa Abinoamu.’

13 “Kenaka anthu okhulupirika anatsatira atsogoleri awo;
anthu a Yehova anapita
kukamenyera Yehova nkhondo
kulimbana ndi adani amphamvu.
14 Anakalowa m’chigwa kuchokera ku Efereimu;

akutsatira iwe Benjamini ndi abale ako.
Akulu a ankhondo anachokera ku Makiri,
ndipo onyamula ndodo ya udindo anachokera ku Zebuloni.
15 Olamulira a Isakara anali pamodzi ndi Debora;
inde, anthu ochokera ku Isakara anatsatanso Baraki,
ndipo anathamangira ku chigwa akumutsatira.
Koma pakati pa mafuko a Rubeni
panali kusinkhasinkha mtima kwambiri osadziwa chenicheni choyenera kuchita.
16 Chifukwa chiyani munangokhala ku makola a nkhosa n'kumangomvetsera
zitoliro zoyitanira nkhosa?
Pakati pa anthu a fuko la Rubeni
panali kusinkhasinkha mtima kwambiri osadziwa chenicheni choyenera kuti achite.
17 Agiliyadi anatsala pa tsidya la Yorodani.
Ndipo n'chifukwa chiyani anthu afuko la Dani anatsarira m'sitima za pa madzi?
Aseri anali pa gombe la Nyanja;
anangokhala m'madooko mwawo.
18 Azebuloni ndi anthu amene anayika moyo wawo m'zoopsa.
Nawonso anthu a fuko la Nafutali anayika miyoyo yawo pa chiswe pomenya nkhondo pamwamba pa mapiri.

19 "Mafumu anabwera, anachita nkhondo;
mafumu Akanaani anachita nkhondo
ku Tanaki pafupi ndi madzi a ku Megido,
koma sanatengeko zofunkha zasiliva.
20 Ngakhalenso nyenyezi zakumwamba zinachita nkhondo,
zinathira nkhondo Sisera, zikuyenda m'njira zake.
21 Mtsinje wa Kisoni unawakokolola,
chigumula cha mtsinje wa Kisoni chinawakokolola.
Mtima wanga, yenda mwamphamvu, limbika!
22 Ndipo ziboda za ng'ombe zazimuna zinachita phokoso lalikulu,
akavalo ali pa liwiro, akuthamanga kwambiri.
23 Mngelo wa Yehova anati 'Tembererani Merozi.'
'Tembererani nzika zake mwaukali,
chifukwa sanabwere kudzathandiza Yehova,
kulimbana ndi adani ake amphamvu.'

24 "Akhale wodala kupambana akazi onse,
Yaeli mkazi wa Heberi Mkeni;
inde mwa akazi onse okhala m'dziko, akhale wodala iyeyu.
25 Munthu uja anapempha madzi akumwa, koma iye anamupatsa mkaka;
anamupatsa chambiko m'chikho cha wolemekezeka.
26 Anatenga chikhomo cha tenti m'dzanja lake,
anatenganso nyundo ndi dzanja lake lamanja.
Ndipo anakhoma nacho Sisera, anamuphwanya mutu wake,
ndi kumubowola mu litsipa mwake.
27 Anathifukira ku mapazi a mkaziyo nagwa,
anagwa; iye anagona pamenepo.
Anagwera pa mapazi a mkaziyo, iye anagwa;

pamene anagwera, pamenepo anaferapo.

28 “Amayi ake a Sisera anasuzumira pa zenera;
nafuwula mokweza kuti,
‘N’chifukwa chiyani galeta lake lachedwa kufika?
N’chifukwa chiyani phokoso la magaleta ake silikumveka?’
29 Amayi ake anzeru kwambiri anamuyankha,
ndithudi, mwiniwake anadziyankha yekha kuti,
30 ‘Kodi iwo sakufunafuna zofunkha kuti agawane;
akugawana wankhondo aliyense mtsikana mmodzi kapena awiri.
Sisera akumupatsa zofunkha:
zovala zonyikidwa mu utoto,
zoti ndizivala m’khosi
zovala zopeta zonyika mu utoto, ndi zopeta zomavala m’khosi?’

31 “Choncho Yehova! adani anu onse awonongeke,
koma iwo amene amakukondani inu akhale ngati dzuwa
pamene lituluka ndi mphamvu zake.”
Ndipo dziko linakhala pa mtendere zaka makumi anayi.

# 6

*Gideoni*

1 Aisraeli anachitanso zinthu zoyipira Yehova, choncho Yehova
anawapereka m’manja mwa Amidiyani kwa zaka zisanu ndi ziwiri.
2 Amidiyani anapondereza Aisraeli. Tsono chifukwa cha Amidiyaniwa,
Aisraeli anakonza malo obisalamo m’mapiri ndi m’mapanga. Anaman-
ganso malinga. 3 Aisraeli amati akadzala mbewu, Amidiyani, Aamaleki
ndi anthu ena akummawa amabwera ndi kudzawathira nkhondo. 4 Iwo
anamanga misasa m’dzikomo ndi kuwononga zokolola zawo zonse mpaka
ku Gaza, ndipo sanawasiyireko chamoyo chilichonse Aisraeliwo, kaya
nkhosa kapena ng’ombe ndi bulu yemwe. 5 Iwo ankabwera ndi zoweta
zawo ndi matenti awo omwe. Ankabwera ambiri ngati dzombe, motero
kuti kunali kovuta kuwawerenga anthuwo ndi ngamira zawo. Tsono iwo
ankabwera ndi kuwononga dziko lonse. 6 Aisraeli anasauka chifukwa cha
Amidiyani ndipo analirira kwa Yehova kuti awathandize.
7 Pamene Aisraeli analirira kwa Yehova chifukwa cha Amidiyaniwo, 8 Iye
anawatumizira mneneri amene anati, “Yehova Mulungu wa Israeli akuti,
‘Ndine amene ndinakutsogolerani kuchokera ku Igupto. Ndinakutulutsani
m’dziko la ukapolo. 9 Ine ndinakupulumutsani ku ulamuliro wa Igupto ko-
manso m’manja mwa amene amakuzunzani. Ndinawathamangitsa adani
anu inu mukufika, ndikukupatsani dziko lawo.’ 10 Ndipo ndinakuwuzani
kuti, ‘Ine ndine Yehova Mulungu wanu; musapembedze Milungu ya
Aamori amene mukukhala m’dziko lawo.’ Koma inu simunandimvere.”
11 Tsiku lina mngelo wa Yehova anabwera ku Ofura ndi kukhala pansi
pa tsinde pa mtengo wa thundu umene unali wa Yowasi Mwabiezeri.
Tsono Gideoni, mwana wake n’kuti pa nthawiyo akupuntha tirigu m’malo
ofinyira mphesa mowabisalira Amidiyani. 12 Tsono mngelo wa Yehova
uja anamuonekera Gideoni nati kwa iye, “Yehova ali nawe, iwe munthu
wamphamvu ndi wolimba mtima.”
13 Gideoni anayankha, “Koma mbuye wanga, ngati Yehova ali nafedi,
n’chifukwa chiyani zonsezi zationekera? Nanga ntchito zake zodabwitsa

zimene makolo athu anatiwuza pamene anati, ‘Yehova anatitulutsa ku
dziko la Igupto,’ zili kuti? Koma tsopano Yehova watitaya ndi kutipereka
m’manja mwa Amidiyani.”

14 Yehova anamuyang’ana namuwuza kuti, “Pita ndi mphamvu zomwe
uli nazo, ukapulumutse Aisraeli m’manja mwa Amidiyani. Kodi si ndine
amene ndakutuma?”

15 Koma Gideoni anafunsa kuti, “Kodi Ambuye anga ine ndingapulu-
mutse bwanji Israeli? Mbumba yanga ndi yopanda mphamvu mu fuko la
Manase, ndiponso ine ndine wamng’ono kwambiri m’banja mwa abambo
anga.”

16 Yehova anamuyankha kuti, “Ine ndidzakhala nawe, ndipo
Amidiyaniwo udzawagonjetsa ngati munthu mmodzi.”

17 Gideoni anati, “Ngati tsopano mwandikomera mtima, ndionetseni
chizindikiro kusonyeza kuti ndinudi mukuyankhula ndi ine. 18 Chonde
musachoke msanga mpaka nditabwerera kwa inu ndi chopereka changa
cha chakudya kudzachipereka kwa inu.”

Ndipo Yehova anamuwuza kuti, “Ine ndikudikira mpaka utabweranso.”

19 Gideoni analowa m’nyumba, ndipo anakakonza mwana wambuzi,
nakonzanso makeke wopanda yisiti a ufa wa makilogalamu khumi.
Nayika nyamayo m’dengu ndipo msuzi wake anawuthira mu m’phika.
Anabwera nazo ndi kukazipereka kwa mngelo uja pa tsinde pa mtengo
wa thundu paja.

20 Mngelo wa Mulungu anamuwuza iye kuti, “Tenga nyamayi pamodzi
ndi makekewa, uziyike pa mwala uwu ndi kuthirapo msuziwu.” Ndipo
Gideoni anatero. 21 Mngelo wa Yehova anatenga msonga ya ndodo imene
inali m’manja mwake nakhudza nayo nyama ndi makeke aja. Nthawi
yomweyo moto unabuka pa thanthwepo ndi kupsereza nyama yonse ndi
makeke aja. Ndipo mngelo wa Yehova sanaonekenso. 22 Apo Gideoni
anazindikira kuti analidi mngelo wa Ambuye, ndipo anati, “Kalanga ine
Yehova Wamphamvuzonse! Ine ndaona mngelo wa Yehova ndi maso!”

23 Koma Yehova anamuwuza kuti, “Mtendere ukhale ndi iwe! Usachite
mantha, sufa ayi.”

24 Choncho Gideoni anamanga guwa lansembe la Yehova pamenepo
ndipo analitcha kuti, Yehova ndiye mtendere. Kufikira lero lino guwali
lilipo ku Ofura wa Mwabiezeri.

25 Usiku womwewo Yehova anati kwa Gideoni, “Tenga ng’ombe ya
mphongo ya abambo ako, ng’ombe ina yachiwiri ya zaka zisanu ndi ziwiri
ndipo ugwetse guwa la Baala limene abambo ako ali nalo, ndi kugwetsanso
fano la Asera limene lili pafupi pake. 26 Kenaka umangire Yehova Mulungu
wako guwa lansembe ndi miyala yoyala bwino pamwamba pa chiwunda
chimenecho. Utenge ng’ombe ya mphongo yachiwiri ija ndipo uyipereke
ngati nsembe yopsereza pogwiritsa ntchito mitengo ya fano la Asera imene
udule ngati nkhunizo.”

27 Choncho Gideoni anatenga antchito ake khumi nachita monga Yehova
anamuwuzira. Ndipo popeza ankaopa anthu a pa banja lake ndiponso
anthu a m’mudzimo sanachite zimenezi masana koma usiku.

28 Anthu a mu mzindamo atadzuka m’mamawa anangoona guwa la
Baala litagwetsedwa ndi fano la Asera limene linali pamwamba pake
litadulidwa ndiponso ng’ombe yamphongo yachiwiri ija itaperekedwa
ngati nsembe yopsereza pa guwa limene linamangidwa lija.

29 Iwo anafunsana wina ndi mnzake, “Wachita zimenezi ndani?”

Atafufuza ndi kufunsafunsa, analingalira kuti, “Gideoni mwana wa Yowasi ndiye wachita zimenezi.”

30 Ndipo anthuwo anawuza Yowasi kuti, “Tulutsa mwana wako, ayenera kufa chifukwa wagumula guwa lansembe la Baala ndipo wadula fano la Asera lomwe linali pamwamba pake.”

31 Koma Yowasi anawuza anthu amene anamuzungulirawo kuti, “Kodi inu mukuti mukhale woyankhulira Baala mlandu? Kodi ndinu amene mukuti mumupulumutse? Amene akufuna kumumenyera nkhondo Baala akhala atafa pofika mmawa! Ngati Baalayo ndi mulungudi, musiyeni adzimenyere yekha nkhondo popeza munthu wina wamugwetsera guwa
lansembe lake.” 32 Choncho tsiku limenelo Gideoni anatchedwa, Yeru-Baala, kutanthauza kuti, “Baala alimbana naye, popeza anagwetsa guwa lake la nsembe.”

33 Tsopano Amidiyani, Amaleki ndi anthu ena akummawa anasonkhana ndipo atawoloka Yorodani anakamanga zinthando za nkhondo ku chigwa
cha Yezireeli. 34 Ndipo Mzimu wa Yehova unatsikira pa Gideoni, ndipo
anayimba lipenga kuyitana Abiezeri kuti amutsatire iye. 35 Iye anatumiza amithenga m'dziko lonse la Manase kuti akamenye nkhondo ndipo Amanase anayitanidwanso kuti amutsate. Anatumanso amithenga kwa Aseri, Azebuloni ndi Anafutali, ndipo onsewo anapita kukakumana naye.

36 Gideoni anati kwa Mulungu, “Ngati mudzapulumutsa Israeli ndi
dzanja langa monga mwalonjezeramu, 37 onani, ine ndiyala ubweya wankhosa pa malo opunthira tirigu. Ngati mame adzagwera pa ubweya wankhosa pokhapa, pa nthaka ponse pakhala powuma, ndiye ndidziwa kuti mudzapulumutsadi Israeli ndi dzanja langa monga mwanenera.”
38 Ndipo zimenezi zinachitikadi. Gideoni atadzuka m'mamawa ndi kuwufinya ubweya uja, anafinya madzi odzaza mtsuko.

39 Kenaka Gideoni anati kwa Mulungu, “Musandikwiyire. Mundilole ndiyankhule kamodzi kokhaka. Ndiyeseko kamodzi kokha ndi ubweyawu kuti pa ubweya pokhapa pakhale powuma koma pa nthaka ponse pakhale
ponyowa ndi mame.” 40 Ndipo Mulungu anachita zomwezo usiku umenewo. Pa ubweya pokha panali powuma, koma pa nthaka ponse panagwa mame.

# 7

## *Gideoni Agonjetsa Amidiyani*

1 Yeru-Baala (Gideoni) ndi anthu ake onse anadzuka m'mamawa nakamanga misasa pambali pa kasupe ku Harodi. Misasa ya Amidiyani
inali m'chigwa kumpoto kwa phiri la More. 2 Yehova anati kwa Gideoni, “Anthu uli nawowa andichulukira kwambiri kuti ndigonjetse Amidiyani chifukwa Aisraeli angamadzitukumule pamaso panga ndi kumanena kuti,
‘Tadzipulumutsa ndi mphamvu zathu.’ 3 Tsono lengeza kwa anthu kuti, ‘Aliyense amene akuchita mantha ndi kunjenjemera abwerere kwawo, ndipo achoke kuno ku phiri la Giliyadi.’ ” Choncho anthu 22,000 anachoka, ndipo anatsalira anthu 10,000.

4 Koma Yehova anawuza Gideoni kuti, “Anthuwa achulukabe. Uwatenge upite nawo ku mtsinje ndipo ndikawayesa kumeneko m'malo mwako. Ndikadzanena kuti, ‘Uyu apite nawe’ adzapita nawe; koma ndikanena kuti ‘Uyu asapite nawe,’ sadzapita nawe.”

5 Choncho Gideoni anatenga anthuwo ndi kupita nawo ku madzi. Kumeneko Yehova anamuwuza kuti, “Amene amwe madzi mokhathira ndi

manja ngati galu uwayike pawokha, ndipo amene amwe atagwada pansi
uwayikenso pawokha.” 6 Ndipo anthu 300 anamwa mokhathira, pamene
ena onse anagwada pansi pakumwa.
7 Yehova anati kwa Gideoni, “Ndi anthu 300 amene anamwa madzi
mokhathira ndi manja awo ndidzakupulumutsani ndipo ndidzapereka
Amidiyani m’manja mwanu. Koma anthu ena onse apite ku nyumba
kwawo.” 8 Choncho analola anthu ena onse kuti apite ku nyumba
zawo kupatula anthu 300 osankhika aja. Iwowa anatenga zakudya ndi
malipenga a anthuwo.
Ndipo misasa ya ankhondo Amidiyani inali kumunsi kwa chigwa.
9 Usiku umenewo Yehova anati kwa Gideoni, “Dzuka, pita kachite nkhondo
ku misasayo, chifukwa ndayipereka m’manja mwako. 10 Ngati ukuopa,
upite ku msasako ndi Pura wantchito wako, 11 ndipo ukamvere zimene
akunena ndipo pambuyo pake udzalimba mtima ndi kupita kukayithira
nkhondo misasayo.” Choncho iye ndi wantchito wake Pura anapita
kumbali ina ya msasawo kumene kunali ankhondo. 12 Amidiyani,
Aamaleki ndi anthu ena onse akummawa anadzaza chigwa chonse ngati
dzombe. Ngamira zawo zinali zambiri zosawerengeka ngati mchenga wa
m’mbali mwa nyanja.
13 Gideoni atafika anangomva munthu wina akuwuza mnzake mal-
oto ake kuti, “Ine ndinalota nditaona dengu la buledi wa barele
likugubuduzika kupita ku misasa ya Amidiyani. Litafika linawomba tenti
moti inagwa ndi kuphwasukaphwasuka.”
14 Ndipo mnzakeyo anamuyankha kuti, “Iyi ndi nkhondo ya Gideoni
mwana wa Yowasi, wa ku Israeli. Mulungu wapereka Amidiyani pamodzi
ndi ankhondo ake onse m’dzanja mwake.”
15 Gideoni atamva za malotowo ndi kumasulira kwake, anapembedza
Mulungu. Kenaka anabwerera ku msasa wa Israeli nawawuza kuti,
“Dzukani popeza Yehova wapereka msasa wa Midiyani m’manja mwanu.”
16 Anawagawa anthu 300 aja magulu atatu, nawapatsa malipenga m’manja
mwawo ndi mbiya zimene m’kati mwake munali nsakali zoyaka.
17 Anawuza anthuwo kuti, “Muzikayang’ana ine ndi kuchita zimene
ndizikachita. Ndikakafika kumalire a msasa, mukachite zomwe ndikachita
ine. 18 Ndikadzaliza lipenga ndi onse amene ali ndi ine, inunso mukalize
malipenga kumbali zonse za misasa yonse ndi kufuwula kuti, ‘Lupanga la
Yehova ndi la Gideoni.’ ”
19 Choncho Gideoni pamodzi ndi amuna 100 omwe anali nawo anafika
ku malire a msasa pakati pa usiku, alonda atangosinthana kumene. Iwo
analiza malipenga awo ndi kuphwanya mbiya zimene zinali m’manja
mwawo. 20 Magulu awiri ena aja anayimbanso malipenga ndi kuswa
mbiya zawo. Aliyense ananyamula nsakali ya moto ku dzanja lamanzere
ndi lipenga ku dzanja lamanja ndipo anafuwula kuti, “Lupanga la Yehova
ndi la Gideoni.” 21 Aliyense anayima pa malo pake kuzungulira misasa.
Ankhondo a m’misasa muja anadzuka nayamba kuthawa akufuwula.
22 Anthu 300 aja ataliza malipenga, Yehova anawasokoneza ankhondo
a Midiyani aja motero kuti ankamenyana okhaokha. Ankhondowo
anathawira ku Beti-Sita cha ku Zerera mpaka ku malire a Abeli-Mehola
pafupi ndi Tabati. 23 Aisraeli a fuko la Nafutali, fuko la Aseri, ndi fuko
lonse la Manase anayitanidwa, ndipo iwo anathamangitsa Amidiyaniwo.
24 Gideoni anatumiza amithenga ku dziko lonse la ku mapiri la Efereimu
kukanena kuti, “Tsikani mumenyane ndi Amidiyani ndipo mulande
madooko awo owolokera mpaka ku Beti-Bara.”

Choncho anthu onse a fuko la Efereimu anasonkhana ndipo analanda
madooko awo owolokera mpaka ku Betibaala. 25 Iwo anagwiranso
atsogoleri awiri a nkhondo a Amidiyani, Orebu ndi Zeebu. Anapha Orebu
ku thanthwe la Orebu, koma Zeebu anamuphera ku malo ofinyira mphesa
ku Zeebu pothamangitsa Amidiyani. Mitu ya Orebu ndi Zeebu anabwera
nayo kwa Gideoni kutsidya kwa Yorodani.

# 8

*Zeba ndi Zalimuna*

1 Aefereimu anafunsa Gideoni kuti, "N'chifukwa chiyani watichita
zimenezi? Bwanji sunatiyitane pamene umakamenyana ndi Amidiyani?"
Iwo anamudzudzula kwambiri.

2 Koma iye anawayankha kuti, "N'chiyani ndachita kuyerekeza ndi
zimene mwachita inu? Kodi zimene mwachita inu Aefereimu si zazikulu
kuposa zimene fuko langa la Abiezeri lachita? 3 Mulungu wapereka
mafumu a Midiyani, Orebu ndi Zeebu m'manja mwanu. Ndachita chiyani
kuyerekeza ndi zimene mwachita inu?" Atanena izi, anthuwo mitima
yawo inatsika.

4 Gideoni anafika ndi kuwoloka mtsinje wa Yorodani pamodzi ndi
anthu 300 amene anali naye. Ngakhale kuti anali otopa anapirikitsabe
adani awo. 5 Atafika ku Sukoti anapempha anthu a kumeneko kuti,
"Chonde apatseniko buledi ankhondo angawa pakuti atopa. Koma ine
ndikupirikitsa Zeba ndi Zalimuna, mafumu a Midiyani."

6 Koma atsogoleri a Sukoti anayankha kuti, "Kodi Zeba ndi Zalimuna
mwawagonjetsa kale kuti tipatse buledi ankhondo akowa?"

7 Gideoni anayankha kuti, "Mwatero! Yehova akapereka Zeba ndi
Zalimuna m'dzanja langa, ndidzakukwapulani ndi matsatsa a minga ya
m'chipululu."

8 Atachoka pamenepo anapita ku Penueli ndipo anapemphanso buledi
kwa anthu a kumeneko, koma iwo anamuyankha monga anayankhira an-
thu a ku Sukoti aja. 9 Gideoni anawawuzanso kuti, "Ndikamadzabwerera
nditawagonjetsa, ndidzagwetsa nsanja iyi."

10 Nthawi iyi n'kuti Zeba ndi Zalimuna ali ku Karikori ndi ankhondo
pafupifupi 15,000. Amenewa ndiwo anatsalako mwa ankhondo a anthu
akummawa; pakuti anafa ankhondo 120,000. 11 Gideoni anadzera njira
ya anthu a matenti kummawa kwa Noba ndi Yogibeha ndipo anawathira
nkhondo popeza ankhondo awo anali osakonzekera. 12 Zeba ndi Zalimuna,
mafumu awiri a Amidiyani anathawa koma Gideoni anawathamangitsa
mpaka kuwagwira. Koma ankhondo awo onse anathawa ndi mantha.

13 Ndipo Gideoni mwana wa Yowasi, pobwera kuchokera ku nkhondo
anadzera njira ya ku chikweza cha Heresi. 14 Kumeneko iye anagwira
mnyamata wa ku Sukoti ndipo atamufunsa, mnyamatayo anamulembera
mayina a akuluakulu ndi atsogoleri 77 a ku Sukoti. 15 Kenaka Gideoni
anabwera kwa anthu a ku Sukoti ndi kunena kuti, "Awa ndi Zeba ndi
Zalimuna, mafumu awiri munkandinena nawo aja kuti, 'Kodi Zeba ndi
Zalimuna wawagonjetsa kale mmene ukuti tiwapatse buledi anthu ako
otopawa?' " 16 Tsono Gideoni anatenga akuluakulu a mu mzindawo ndipo
anagwira matsatsa a minga za m'chipululu ndi kuwakwapula nawo.
17 Anagwetsa nsanja ya ku Penueli ndi kupha amuna onse a mu mzindawo.

18 Kenaka anafunsa Zeba ndi Zalimuna kuti, "Kodi anthu a ku Tabori
amene munawapha aja anali a maonekedwe otani?" Iwo anayankha kuti,

"Anali anthu a maonekedwe ngati inu. Aliyense ankaoneka ngati mwana
wa mfumu?"
Iwo anayankha kuti, "Anthu ngati inu, aliyense wooneka ngati mwana
wa mfumu."
19 Ndipo Gideoni anayankha kuti, "Ndikulumbira pa Mulungu, mukana-
panda kuwapha nanenso sindikanakuphani. Ndi abale anga amenewo,
ana a amayi anga enieni." 20 Tsono anawuza Yetero, mwana wake
wachisamba kuti, "Tiye, ipha anthu amenewa!" Koma chifukwa Yeteri
anali wamng'ono sanasolole lupanga lake, popeza anachita mantha.
21 Tsono Zeba ndi Zalimuna anawuza Gideoni kuti, "Bwera utiphe ndiwe
chifukwa uli ndi mphamvu za munthu wamkulu." Choncho Gideoni
anapita nawapha natenganso zokongoletsera zimene zinali pa makosi a
ngamira zawo.

### *Efodi ya Gideoni*

22 Aisraeli anati kwa Gideoni, "Inu muzitilamulira, mwana wanu ndi
zidzukulu zanu, chifukwa mwatipulumutsa m'manja mwa Amidiyani."
23 Koma Gideoni anawawuza kuti, "Sindidzakulamulirani, mwana
wanganso sadzakulamulirani. Koma Yehova ndiye adzakulamulirani."
24 Gideoni anatinso, "Ine ndikupemphani chinthu chimodzi. Aliyense wa
inu andipatse ndolo zomwe anafunkha ku nkhondo." (Adani aja anali ndi
ndolo zagolide popeza anali Aismaeli).
25 Iwo anayankha kuti, "Ife tikupatsani ndithu ndolozi." Choncho
anayala chinsalu, ndipo aliyense anaponyapo ndolo zimene anafunkha.
26 Tsono kulemera kwa ndolo zagolide zimene anapereka kunali makilo-
galamu makumi awiri, osawerengera kulemera kwa mphande, mkanda
wam'khosi, zovala zapepo za mafumu a Midiyani ndiponso malamba
azitsulo za m'makosi a ngamira zawo. 27 Gideoni anagwiritsa ntchito
golide uja kupanga efodi, ndipo anakamuyika ku mzinda wake ku Ofura.
Tsono Aisraeli onse anasiya kupembedza Yehova nayamba kupembedza
efodiyo kumeneko. Ichi chinasanduka msampha kwa Gideoni ndi banja
lake lonse.

### *Imfa ya Gideoni*

28 Choncho Amidiyani anagonjetsedwa ndi Aisraeli ndipo sanayeserenso
kuwawukira. Ndipo dzikolo linakhala pa mtendere kwa zaka 40 pamene
Gideoni anali ndi moyo.
29 Yeru-Baala mwana wa Yowasi anapita kukakhala kwawo. 30 Ana a
Gideoni anali 70 popeza anali ndi akazi ambiri. 31 Mdzakazi wake amene
anali ku Sekemu, anabereka naye mwana wamwamuna, amene ana-
mutcha Abimeleki. 32 Gideoni mwana wa Yowasi anamwalira atakalamba
ndipo anayikidwa m'manda a abambo ake, Yowasi ku Ofura mzinda wa
Mwabiezeri.
33 Atangomwalira Gideoni, Aisraeli anayambanso kupembedza Abaala.
Iwo anasandutsa Baala-Beriti kukhala mulungu wawo. 34 Aisraeli
sanakumbukirenso Yehova Mulungu wawo amene anawapulumutsa
m'manja mwa adani awo mbali zonse. 35 Ndiponso sanachite zinthu
zokomera banja la Yeru-Baala (ndiye kuti Gideoni) chifukwa cha zabwino
zonse zimene iye anawachitira.

## 9

### *Abimeleki*

1 Abimeleki mwana wa Yeru-Baala anapita ku Sekemu kwa abale a
amayi ake ndi kukawawuza iwowo ndi fuko lonse la banja la abambo
a amayi ake kuti, 2 “Funsani nzika zonse za ku Sekemu kuno, ‘Chabwino
ndi chiyani kwa inu kuti ana onse makumi asanu ndi awiri a Yeru-Baala
azikulamulirani, kapena kuti azikulamulirani ndi munthu mmodzi basi?’
Kumbukirani kuti ine ndine m’bale wanu weniweni.”

3 Abale a amayi akewo anamuyankhulira mawu amenewa kwa nzika
zonse za ku Sekemu, ndipo mitima ya anthu onse inali pa Abimeleki
chifukwa anati, “Uyu ndi m’bale wathu,” 4 Tsono anamupatsa ndalama
zasiliva 70 za m’nyumba ya chipembedzo ya Baala Beriti. Ndi ndalama
zimenezi Abimeleki analemba anthu achabechabe ndi osasamala kuti
azimutsatira. 5 Anapita ku Ofiri ku mudzi kwa abambo ake ndipo anapha
abale ake makumi asanu ndi awiri, ana a Yeru-Baala pa mwala umodzi.
Koma Yotamu yemwe anali wamng’ono mwa onsewo anapulumuka
chifukwa anabisala. 6 Tsono nzika za ku Sekemu ndi za ku Beti-Milo
zinapita kukasonkhana ku mtengo wa thundu pafupi ndi chipilala cha
ku Sekemu kuti akalonge Abimeleki ufumu.

7 Yotamu atamva izi anapita kukayima pamwamba pa phiri la Gerizimu
ndipo anafuwula nati, “Tandimverani inu anthu a ku Sekemu, kuti
Mulungu akumvereninso. 8 Tsiku lina mitengo inapita kukadzoza mfumu
yawo. Tsono mitengoyo inati kwa mtengo wa olivi, ‘Iwe ukhale mfumu
yathu.’ ”

9 “Koma mtengo wa olivi uja unayankha kuti, ‘Kodi ndisiye mafuta
angawa amene amalemekezera nawo milungu ndi anthu omwe, kuti
ndizikalamulira mitengo?’ ”

10 Apo mitengo inawuza mtengo wa mkuyu kuti, “Bwera ndiwe ukhale
mfumu yathu.”

11 Koma mtengo wa mkuyu unayankha kuti, “Kodi ndisiye chipatso
changa chokoma ndi chozunachi kuti ndizikalamulira mitengo?”

12 Kenaka mitengo ija inawuza mtengo wamphesa kuti, “Bwera ndiwe
kuti ukhale mfumu yathu.”

13 Koma mtengo wamphesa unayankha kuti, “Kodi ine ndisiye vinyo
wangayu, amene amasangalatsa milungu ndi anthu omwe kuti ndizikala-
mulira mitengo?”

14 Pomaliza mitengo yonse inawuza mkandankhuku kuti, “Bwera ndipo
ukhale mfumu yathu.”

15 Mkandankhuku uja unayankha kuti, “Ngati mukufunadi kuti mudzoze
ine kuti ndikhale mfumu yanu, bwerani mudzabisale mu mthunzi
mwangamu, koma ngati simutero, moto utuluka kwa ine ndi kupsereza
mikungudza ya ku Lebanoni.”

16 Yotamu anatinso, “Kodi mukuti munaonetsadi kuona mtima ndi
kukhulupirika podzoza Abimeleki kukhala mfumu? Kodi mukuti mu-
nachitira ulemu Yeru-Baala ndi banja lake poganizira ntchito zimene
anachita? 17 Kodi suja abambo anga anakumenyerani nkhondo ndi kuyika
moyo wawo pa chiswe kuti akupulumutseni m’manja mwa Amidiyani?
18 Koma lero inu mwawukira banja la abambo anga. Mwapha ana ake
70 pa mwala umodzi, ndiponso mwalonga ufumu Abimeleki, mwana wa
mdzakazi wake kuti akhale wolamulira anthu a ku Sekemu chifukwa
ndi m’bale wanu. 19 Tsono ngati mukuti zimene mwachitira Yeru-Baala
ndi banja lake mwazichita moona mtima ndiponso mokhulupirika, ndiye
mukondwere ndi Abimeleki, nayenso akondwere nanu! 20 Koma ngati

sichoncho moto utuluke mwa Abimeleki ndi kupsereza anthu a ku Sekemu
ndi Beti-Milo, ndipo moto utulukenso mwa anthu a ku Sekemu ndi Beti-
Milo, ndi kupsereza Abimeleki!”

21 Kenaka Yotamu anathawira ku Beeri nakakhala komweko chifukwa
ankaopa Abimeleki m’bale wake.

22 Abimeleki atalamulira Israeli zaka zitatu, 23 Mulungu anayika chidani
pakati pa Abimelekiyo ndi anthu a ku Sekemu, motero kuti anthu a ku
Sekemu anawukira Abimeleki. 24 Mulungu anachita zimenezi kuti zoyipa
zimene anachitira ana aamuna 70 a Yeru-Baala aja zimubwerere, ndi kuti
magazi awo akhale pa Abimeleki m’bale wawo ndi pa anthu a ku Sekemu
amene anamulimbikitsa mtima kuti aphe abale akewo. 25 Choncho anthu a
ku Sekemu anayika anthu omubisalira pamwamba pa mapiri. Tsono iwo
ankalanda anthu odutsa m’njira imeneyo zinthu zawo ndipo Abimeleki
anamva zimenezi.

26 Gaali mwana wa Ebedi anasamukira ku Sekemu ndi abale ake, ndipo
anthu a ku Sekemuko anamukhulupirira iye. 27 Anthuwo anapita ku
munda kukathyola mphesa ndi kuzifinya, ndipo anachita chikondwerero
m’nyumba ya milungu yawo. Anthuwo akudya ndi kumwa, ankatember-
era Abimeleki. 28 Ndipo Gaali mwana wa Ebedi anati “Kodi Abimeleki
ndi ndani, ndipo n’chifukwa chiyani akutilamulira ife Asekemu? Kodi
iyeyu si mwana wa Yeru-Baala ndipo womuthandiza wake si Zebuli?
Tiyeni titumikire anthu a ku Hamori, kholo la fuko la Sekemu! Nanga
n’chifukwa chiyani tikutumikira Abimeleki? 29 Anthu a mu mzindawo
akanakhala pansi pa ulamuliro wanga, ndikanamuchotsa Abimelekiyu.
Ndikanamuwuza Abimeleki kuti, ‘Wonjeza ankhondo ako ndipo ubwere
tidzamenyane!’ ”

30 Zebuli amene ankalamulira mzindawo atamva zimene Gaali mwana
wa Ebadi ananena, anakwiya kwambiri. 31 Anatumiza amithenga kwa
Abimeleki, kukanena kuti, “Gaali mwana wa Ebedi ndi abale ake abwera
ku Sekemu ndipo akuwutsa mitima ya anthu a mu mzindawo kuti
akuwukireni inu. 32 N’chifukwa chake usiku womwe uno inu ndi anthu
anu mupite, mukabisale m’minda. 33 Mmawa dzuwa likutuluka, mudzuke
ndi kukathira nkhondo mzindawo. Gaali ndi anthu amene ali naye
akamadzabwera kuti alimbane ndi inu, inu mudzathane nawo monga
mmene mungachitire.”

34 Choncho Abimeleki ndi ankhondo ake onse anadzuka usiku
nakabisalira mzinda wa Sekemu m’magulu anayi. 35 Gaali mwana wa
Ebedi anatuluka nakayima pa khomo pa chipata cha mzinda pamene
Abimeleki ndi ankhondo ake anatuluka ku malo kumene anabisala kuja.

36 Gaaliyo atawaona, anawuza Zebuli kuti, “Taona anthu akutsika
kuchoka pamwamba pa mapiri.”

Koma Zebuli anayankha kuti, “Zimene mukuonazo ndi zithunzi za
mapiri chabe osati anthu.”

37 Koma Gaaliyo anayankhulanso kuti, “Taona anthu akutsika kuchokera
pakati pa phiri, ndipo gulu lina likubwera kuchokera ku mtengo wa
thundu wa owombeza mawula.”

38 Ndipo Zebuli anamufunsa iye kuti, “Pakamwa pako paja pali kuti
tsopano, iwe amene umanena kuti, Abimeleki ndaninso kuti ife timutu-
mikire? Kodi amenewa si anthu aja umawanyozawa? Tsopano tuluka
ukamenyane nawo.”

39 Choncho Gaaliyo anatuluka akutsogolera anthu a ku Sekemu kuka-
menyana ndi Abimeleki. 40 Koma Abimeleki anamuthamangitsa ndipo

Gaala anathawa. Ambiri a ankhondo ake anagwa napwetekeka njira
yonse mpaka ku chipata cha mzinda. [41] Abimeleki anakhala ku Aruma,
ndipo Zebuli anathamangitsa Gaali pamodzi ndi abale ake, kuwatulutsa
mu Sekemu.

[42] Mmawa mwake anthu a ku Sekemu anapangana zopita ku minda,
ndipo Abimeleki anamva zimenezi. [43] Tsono Abimeleki anatenga anthu
ake, nawagawa magulu atatu ndi kukabisala m'minda. Ataona anthu
akutuluka mu mzindawo, iye anapita kukalimbana nawo ndipo onsewo
anawapha. [44] Abimeleki pamodzi ndi magulu ake anathamangira
kutsogolo nakawakhalira pa chipata cha mzinda. Ndipo magulu awiri
ena aja anathamangira anthu amene anali m'minda ndi kuwapha onse.
[45] Abimeleki anawuthira nkhondo mzindawo tsiku lonse. Kenaka anawu-
landa ndi kupha nzika zonse za mu mzindamo. Anawuwonongeratu
mzindawo nawuwaza mchere.

[46] Anthu a mu nsanja ya Sekemu atamva zimenezi, anakalowa mu linga
la nyumba yopembedzeramo Baala-Beriti. [47] Abimeleki anamva kuti anthu
ena asonkhana kumeneko. [48] Choncho Abimeleki pamodzi ndi anthu
ake onse anapita ku phiri la Zalimoni. Kumeneko anatenga nkhwangwa
nadula nthambi za mitengo. Ananyamula nthambi zija pa phewa pake.
Tsono anawuza anthu aja kuti, "Zimene mwaona ine ndikuchita, inunso
mufulumire kuchita monga ndachitiramu." [49] Tsono aliyense anadula
nthambi zake, natsatira Abimeleki. Anakawunjika nthambi zija pa linga
paja, kenaka ndi kuliyatsa moto. Choncho anthu onse a ku nsanja ya
Sekemu anafa. Analipo anthu pafupifupi 1,000, amuna ndi akazi.

[50] Kenaka Abimeleki anapita ku Tebezi. Anakawuzungulira mzindawo
ndi kuwulanda. [51] Koma mu mzindamo munali nsanja yolimba. Anthu
onse a mu mzindamo amuna ndi akazi anathawira mu nsanjayo, nadzit-
sekera m'kati. Ndipo anakwera ku denga la nsanjayo. [52] Abimeleki anapita
ku nsanjayo nathira nkhondo. Anafika pafupi ndi chitseko cha nsanja ija
kuti ayitenthe. [53] Koma mkazi wina anaponya mwala wa mphero pa mutu
wa Abimeleki ndi kuswa chibade cha mutuwo.

[54] Mwamsanga Abimeleki anayitana mnyamata womunyamulira zida
za nkhondo namuwuza kuti, "Solola lupanga lako undiphe kuti anthu
asadzanene kuti, 'Mkazi ndiye anamupha.' " Choncho wantchito wake
anamubayadi mpaka kutulukira kunja lupangalo ndipo anafa. [55] Aisraeli
ataona kuti Abimeleki wafa, anapita kwawo.

[56] Mmenemu ndi mmene Mulungu analipsirira tchimo la Abimeleki
limene anachitira abambo ake pakupha abale ake 70 aja. [57] Mulungu
anawalanganso anthu a ku Sekemu chifukwa cha kuyipa kwawo konse.
Ndipo matemberero a Yotamu mwana wa Yeru-Baala anawagweradi.

# 10

*Tola*

[1] Atafa Abimeleki panabwera Tola mwana wa Puwa, mdzukulu wa Dodo
kudzapulumutsa Aisraeli. Iyeyu anali wa fuko la Isakara ndipo ankakhala
ku Samiri m'dziko la mapiri la Efereimu. [2] Iye anatsogolera Aisraeli kwa
zaka 23, ndipo anamwalira ndi kuyikidwa ku Samiri.

*Yairo*

[3] Atafa Tola panabwera Yairi wa ku Giliyadi, amene anatsogolera Israeli
kwa zaka 22. [4] Iyeyu anali ndi ana aamuna makumi atatu, amene

ankakwera pa abulu makumi atatu. Iwo anali ndi mizinda makumi atatu m'dziko la Giliyadi, imene mpaka lero ikutchedwa kuti Havoti Yairi.
5 Atamwalira Yairi anayikidwa m'manda ku Kamoni.

### *Yefita*

6 Aisraeli anachitanso zoyipira Yehova. Iwo anatumikira Abaala ndi Asitoreti, milungu ya ku Aramu, Sidoni, Mowabu, Aamoni ndi Afilisti.
Choncho analeka osatumikiranso Yehova. 7 Tsono Yehova anapsera mtima
Aisraeli ndipo anawapereka m'manja mwa Afilisti ndi Aamoni. 8 Iwowa anawagonjetseratu Aisraeli m'chaka chimenechi, ndipo kwa zaka 18 anakhala akusautsa Aisraeli onse amene anali pa tsidya la Yorodani,
m'dziko la Aamori ku Giliyadi. 9 Aamori anawoloka mtsinje wa Yorodani
kukathira nkhondo mafuko a Yuda, Benjamini ndi Efereimu kotero kuti
Israeli anavutika kwambiri. 10 Kenaka Aisraeli analira kwa Yehova kuti, "Ife takuchimwirani popeza tasiya Inu Mulungu wathu ndi kutumikira Abaala."

11 Yehova anawafunsa kuti, "Suja ine ndinakupulumutsani kwa Aigupto,
Aamori, Aamoni ndi Afilisti? 12 Ndiponso pamene Asidoni, Aamaleki ndi Amoni anakuzunzani, inu n'kulirira kwa ine suja ndinakupulumutsani
kwa anthu amenewa? 13 Komabe inu mwandikana ndipo mukutumikira
milungu ina. Choncho sindidzakupulumutsaninso. 14 Pitani kalireni kwa milungu imene mwayisankha. Iyoyo ikupulumutseni ku mavuto anuwo."

15 Koma Aisraeli anayankha Yehova kuti, "Ife tachimwa. Tichitireni chimene mukuona kuti ndi chabwino, koma chonde tipulumutseni lero
lokha." 16 Ndipo anachotsa milungu ya chilendo pakati pawo ndi kuyamba kutumikira Yehova. Ndipo Yehova anamva chisoni poona mmene Aisraeli ankazunzikira.

17 Tsono Aamoni anasonkhana ndi kumanga zithando za nkhondo ku Giliyadi. Nawonso Aisraeli anasonkhana ndi kumanga zithando zawo
za nkhondo ku Mizipa. 18 Kenaka anthuwo ndi atsogoleri a Agiliyadi
anayamba kufunsana kuti, "Kodi ndi munthu wotani amene atayambe kuthira nkhondo Aamoni? Iyeyu adzakhala mtsogoleri wolamulira anthu onse a ku Giliyadi."

## 11

1 Yefita wa ku Giliyadi anali wankhondo wa mphamvu. Iyeyu amayi ake
anali mkazi wachiwerewere, ndipo abambo ake anali Giliyadi. 2 Mkazi wake wa Giliyadi anabereka naye ana aamuna. Tsono ana amenewa
atakula anapirikitsa Yefita ndi kumuwuza kuti, "Sudzalandirako cholowa
m'nyumba ya abambo athu chifukwa ndiwe mwana wa mkazi wina."
3 Choncho Yefita anathawa kuchoka kwa abale ake ndi kukakhala m'dziko la Tobu. Kumeneko anakakopa ndi kusonkhanitsa anthu achabechabe ndipo anatuluka pamodzi kukasakaza zinthu.

4 Patapita nthawi Aamoni anadzachita nkhondo ndi Israeli. 5 Tsono pamene Aamoni ankathira nkhondo Aisraeli, akuluakulu a ku Giliyadi
anapita kukamutenga Yefita ku dziko la Tobu. 6 Iwo anati kwa iye, "Bwera ukhale mkulu wathu wankhondo kuti timenyane ndi Amoni."

7 Yefita anawawuza Agiliyadi kuti, "Kodi inu suja munkadana nane ndi kundithamangitsa ku nyumba ya abambo anga? N'chifukwa chiyani lero mwabwera kwa ine pamene muli pa mavuto?"

8 Akuluakulu a ku Giliyadi aja anamuyankha kuti, “Chimene tabwerera kwa iwe ndi chakuti upite nafe kukamenyana ndi Aamoni, ndipo udzakhala wolamulira wa onse okhala mu Giliyadi.”

9 Yefita anawayankha akuluakulu a ku Giliyadi kuti, “Ngati mundibwezeranso kwathu kuti ndikachite nkhondo ndi Aamoni ndipo Yehova n’kukandithandiza kuwagonjetsa, ndidzakhaladi wokulamulirani?”

10 Akuluakulu a ku Giliyadi anamuyankha kuti, “Yehova akhale mboni
pakati pa inu ndi ife, ngati sitidzachita monga mwa mawu anu.”
11 Choncho Yefita anapita nawo akuluakulu a ku Giliyadi aja, ndipo anthu a kumeneko anamusandutsa kukhala wowalamulira ndi mkulu wankhondo. Tsono Yefita anabwerezanso mawu omwewa pamaso pa Yehova ku Mizipa.

12 Kenaka Yefita anatuma amithenga kwa mfumu ya Aamoni ndi funso lakuti, “Kodi ife takuchimwirani chiyani kuti muzichita nkhondo ndi dziko langa?”

13 Ndipo mfumu ya Aamoni inayankha amithenga a Yefita aja kuti, “Pamene Israeli amatuluka kuchokera mu Igupto, analanda dziko langa kuyambira ku mtsinje wa Arinoni mpaka ku mtsinje wa Yaboki mpakanso ku mtsinje wa Yorodani. Tsopano mundibwezere dziko langa mwamtendere.”

14 Yefita anatumizanso amithenga akewo kwa mfumu ya Aamoni
15 kukanena kuti,

Yefita akuti, “Israeli sanalande dziko la Mowabu kapena dziko la
Aamoni. 16 Koma pamene Aisraeli ankachoka ku Igupto anadzera
njira ya ku chipululu mpaka ku Nyanja Yofiira nakafika ku Kadesi.
17 Kenaka Israeli anatumiza amithenga kwa mfumu ya ku Edomu kuti, ‘Chonde tiloleni kuti tidutse m’dziko lanu,’ Koma mfumu ya ku Edomu sinamvere zimenezo. Aisraeli anatumizanso amithenga kwa mfumu ya ku Mowabu, ndipo iyo inakananso. Choncho Israeli anakhala ku Kadesi.

18 “Pambuyo pake, Aisraeli ananyamuka ulendo kudzera ku chipululu nazungulira dziko la Edomu ndi dziko la Mowabu, ndipo anafika ku mmawa kwa dziko la Mowabu ndi kumanga zinthando zawo ku mbali ina ya mtsinje wa Arinoni. Iwo sanalowe m’dziko la Mowabu, chifukwa mtsinje wa Arinoni ndiwo unali malire a dziko la Mowabu.

19 “Pambuyo pake Israeli anatumiza amithenga kwa Sihoni mfumu ya Aamori, amene amalamulira ku Hesiboni ndipo anati kwa iye, ‘Chonde
tiloleni kuti tidutse m’dziko lanu popita kwathu.’ 20 Koma Sihoni
sanalole Israeli kuti adzere m’dziko mwake. M’malo mwake Sihoni anasonkhanitsa ankhondo ake onse nakamanga msasa ku Yahazi ndipo anachita nkhondo ndi Israeli.

21 “Koma Yehova Mulungu wa Israeli anamupereka Sihoni pamodzi ndi anthu ake onse m’manja mwa Israeli, ndipo anawagonjetsa. Choncho Aisraeli analanda dziko lonse la Aamori amene amakhala
m’dzikolo. 22 Analanda dziko lonse kuchokera ku Arinoni mpaka ku Yaboki ndiponso kuchokera ku chipululu mpaka ku mtsinje wa Yorodani.

23 “Ndiye kuti Yehova Mulungu wa Aisraeli ndiye analanda dziko la Aamori, kuwalandirira anthu ake. Kodi inu mukufuna kutilanda
dzikolo? 24 Bwanji inu osakhazikika m’dziko limene Kemosi mulungu wanu anakupatsani, ifenso tikhazikike m’dziko limene Yehova Mulungu
wathu anatipatsa? 25 Kodi ndinu abwino kuposa Balaki mwana wa Zipori, mfumu ya Mowabu? Kodi iye anakanganapo kapena
kuchita nkhondo ndi Israeli? 26 Pamene Aisraeli ankakhala m’dziko la

Hesiboni ndi m'midzi yake, m'dziko la Aroeri ndi midzi yake, komanso m'mizinda yonse imene ili m'mbali mwa mtsinje wa Arinoni kwa zaka 300, n'chifukwa chiyani inu simunalande malowo nthawi imeneyo?
27 Choncho ine sindinakuchimwireni. Koma inu mukundilakwira pomenyana nane. Yehova woweruza, ndiye aweruze lero mlandu wa pakati pa Aisraeli ndi Aamoni."

28 Koma mfumu ya Aamori, sinasamale mawu amene Yefita anatumiza kwa iyo.

29 Tsono Mzimu wa Yehova unatsikira pa Yefita. Ndipo iye ananya-
muka nadzera ku Giliyadi ndi ku Manase. Anafika ku Mizipa m'dziko
la Giliyadi, ndipo kuchokera kumeneko anapita kukalimbana ndi Aa-
moni. 30 Yefita analumbira kwa Yehova kuti, "Ngati mupereka Aamoni
m'manja mwanga, 31 aliyense amene atuluke pa khomo la nyumba yanga
kudzandichingamira pobwerera nditagonjetsa Aamoni adzakhala wake wa Yehova, ndipo ndidzamupereka kuti akhale nsembe yopsereza."

32 Kenaka Yefita anawolokera kwa Aamoni kukamenya nawo nkhondo,
ndipo Yehova anawaperekadi m'manja mwake. 33 Iye anawononga
mizinda makumi awiri kuchokera ku Ariori mpaka pafupi ndi mzinda wa Miniti. Anapitirira mpaka ku Abeli-Keranimu. Choncho Aisraeli anagonjetsa Aamoni.

34 Pambuyo pake Yefita anabwerera ku nyumba yake. Tsono anangoona mwana wake wamkazi akutuluka kudzamuchingamira akuyimba ng'oma
ndi kuvina. Uyu anali mwana yekhayo wa Yefita. Analibenso mwana
wina wamwamuna kapena wamkazi. 35 Yefita ataona mwana wake
uja, anang'amba zovala zake ndi kulira, "Kalanga ine! Mwana wanga! Wandivulaza kwambiri ndipo iwe ndi gwero la mavuto anga. Ine ndinalumbira kwa Yehova ndi pakamwa pangapa ndipo sindingathe kubweza malumbiro angawo."

36 Mwanayo anayankha kuti, "Abambo, ngati munalonjeza kwa Yehova ndi pakamwa panu, chitani zimene munalonjezera pakuti Yehova
wakuthandizani kulipsira adani anu Amowabu." 37 Anatinso kwa abambo
ake, "Ndikupempheni chinthu ichi: Mundilole ndikayendeyende ku mapiri miyezi iwiri ndizikalira pamodzi ndi anzanga chifukwa ndikufa ndikanali namwali wosadziwa mwamuna."

38 Yefita anamuyankha kuti, "Pita." Ndipo anamulola kuti apite miyezi
iwiri. Tsono anapita kumapiri ndi atsikana anzake kukalira chifukwa cha
unamwali wake. 39 Miyezi iwiri itatha iye anabwerera kwa abambo ake,
ndipo anachitadi zimene analonjeza.

Motero unakhala mwambo wa Aisraeli, 40 kuti atsikana a Israeli
ankapita chaka chilichonse kukalira maliro a mwana wa mkazi wa Yefita, Mgiliyadi uja masiku makumi anayi pa chaka.

# 12

*Yefita ndi Aefereimu*

1 Gulu la nkhondo la fuko la Efereimu linayitanidwa ndipo anawolokera ku Zafoni nakafunsa Yefita kuti, "N'chifukwa chiyani unawoloka kuka-
chita nkhondo ndi Aamoni osatiyitana kuti tipite nawe? Ife tikutenthera m'nyumba mwakomu."

2 Yefita anayankha kuti, "Ine ndi anthu anga tinakangana kwambiri ndi Aamoni. Ndinakuyitanani koma inu simunandipulumutse m'manja
mwawo. 3 Nditaona kuti simundithandiza, ndinayika moyo wanga pa

chiswe ndipo ndinawoloka kukachita nkhondo ndi a Aamoni. Yehova
ananndithandiza ndipo ndinawagonjetsa. Nanga n'chifukwa chiyani
mwabwera kwa ine lero kuti muchite nane nkhondo?"
4 Choncho Yefita anasonkhanitsa anthu a ku Giliyadi ndi kuchita
nkhondo ndi Aefereimu. Ndipo Agiliyadi anagonjetsa Aefereimu chifukwa
Aefereimuwo amati, "Inu a Giliyadi ndinu othawa kuchokera ku Efereimu
ndi pakati pa Amanase." 5 Choncho Agiliyadi analanda Aefereimu
madooko a mtsinje wa Yorodani. Munthu aliyense wothawa ku Efereimu
amati akanena kuti, "Ndiloleni ndiwoloke," Agaliyadi ankafunsa kuti,
"Kodi ndiwe mu Efurati?" Ngati iye ayankha kuti, "Ayi" 6 Ndiye
amamuwuza kuti, "Nena kuti 'Shiboleti.' " Tsono munthuyo akanena kuti
Siboleti popeza samatha kutchula bwino mawuwa, ankamugwira ndi
kumupha pomwepo pa madooko a mtsinje wa Yorodani. Nthawi imeneyo
anaphedwa Aefereimu 42,000.
7 Yefita anatsogolera Israeli zaka zisanu ndi chimodzi. Kenaka Yefita wa
ku Giliyadi anamwalira, ndipo anayikidwa mu mzinda wake ku Giliyadi.

*Ibizani, Eloni ndi Abidoni*

8 Atamwalira Yefita, Ibizani wa ku Betelehemu anatsogolera Israeli.
9 Iye anali ndi ana aamuna makumi atatu ndi ana aakazi makumi atatu.
Anakwatitsa ana ake akaziwo kwa anthu a fuko lina, ndipo ana ake
aamuna aja anawabweretsera atsikana makumi atatu kuti awakwatire
amenenso anali a fuko lina. Ibizani anatsogolera Israeli kwa zaka
zisanu ndi ziwiri. 10 Kenaka Ibizani anamwalira, ndipo anayikidwa mu
Betelehemu.
11 Iye atamwalira, Eloni wa fuko la Zebuloni anakhala mtsogoleri wa
Aisraeli, ndipo anatsogolera Aisraeli kwa zaka khumi. 12 Kenaka Eloni
anamwalira ndipo anayikidwa ku Ayaloni m'dziko la Zebuloni.
13 Iye atamwalira, Abidoni mwana wa Hilelo wochokera ku Piratoni,
anatsogolera Israeli. 14 Iye anali ndi ana aamuna makumi anayi ndi
zidzukulu makumi atatu, amene ankakwera pa abulu 70. Iye anatsogolera
Israeli kwa zaka zisanu ndi zitatu. 15 Ndipo Abidoni mwana wa Hilelo
Mpiratoni uja anamwalira, nayikidwa ku Piratoni, m'dziko la Efereimu,
dziko lamapiri la Aamaleki.

# 13

*Kubadwa kwa Samsoni*

1 Aisraeli anachitanso zinthu zoyipira Yehova, kotero Yehova
anawapereka m'manja mwa Afilisti kwa zaka makumi anayi.
2 Ku Zora kunali munthu wina dzina lake Manowa, wochokera ku fuko
la Dani. Mkazi wake analibe ana popeza anali wosabereka. 3 Mngelo
wa Yehova anaonekera mkaziyo ndipo anati, "Ndinu wosabereka ndipo
mulibedi mwana, komabe mudzakhala ndi pakati ndipo mudzabereka
mwana wamwamuna. 4 Tsono mudzisamale bwino, osamwa vinyo kapena
chakumwa chilichonse choledzeretsa ndiponso musamadye chakudya
chilichonse chodetsedwa, 5 chifukwa mudzakhala ndi pakati ndipo mudz-
abereka mwana wamwamuna. Mwanayo akadzabadwa lumo lisadzapite
pa mutu chifukwa mnyamatayo adzakhala Mnaziri, ndiye kuti wopatulika
kwa Mulungu kuyambira pa nthawi imene adzakhale ali m'chiberekero.
Ndipo adzayamba ntchito yopulumutsa Israeli m'manja mwa Afilisti."

6 Kenaka mayiyo anapita kukawuza mwamuna wake kuti, “Munthu
wa Mulungu anabwera kwa ine, ndipo maonekedwe ake anali ngati
mngelo wa Mulungu, maonekedwe woopsa kwambiri. Ine sindinamu-
funse kumene amachokera, ndipo iyeyo sanandiwuzenso dzina lake.
7 Koma anandiwuza kuti, ‘Mudzakhala ndi pakati ndipo mudzabereka
mwana wamwamuna. Choncho musamamwe vinyo kapena chakumwa
chilichonse choledzeretsa, musamadye chakudya chilichonse choyipit-
sidwa chifukwa mwanayo adzakhala Mnaziri, wopatulika kwa Mulungu
kuyambira pa nthawi imene adzakhale ali m’chiberekero mpaka tsiku la
kufa kwake.’ ”

8 Kenaka Manowa anapemphera kwa Yehova kuti, “Chonde Ambuye,
lolani munthu wa Mulungu amene munamutuma abwerenso kwa ife kuti
adzatiphunzitse zochita ndi mwanayo akadzabadwa.”

9 Mulungu anamva pemphero la Manowa, ndipo mngelo wa Mulungu
anabweranso kwa mkaziyo nthawi imene anali ku munda, koma Manowa
mwamuna wake sanali naye. 10 Tsono mkaziyo anathamanga kukawuza
mwamuna wake kuti, “Wandionekeranso munthu uja amene anabwera
kwa ine tsiku lija.”

11 Choncho Manowa ananyamuka namutsatira mkazi wake. Atafika
kwa munthuyo anamufunsa kuti, “Kodi ndinu munayankhula ndi mkazi
wanga?”

Iye anayankha kuti, “Ndine.”

12 Kenaka Manowa anafunsa kuti, “Tiyerekeze kuti mawu anuwa
akwaniritsidwadi, ndiye mwanayu azidzakhala bwanji ndipo azidzachita
chiyani?”

13 Ndipo mngelo wa Yehova uja anamuyankha kuti, “Zonse zimene
ndinawawuza akazi anuwa asamale ndipo adzazichitedi. 14 Asadzadye
chilichonse chochokera ku mphesa. Asadzamwe vinyo kapena choledz-
eretsa chilichonse, ngakhale kudya chakudya chilichonse chodetsedwa.
Zonse zimene ndinawalamula azisunge bwino.”

15 Manowa anamuwuza mngelo wa Yehova uja kuti, “Chonde dikirani
pang’ono, timati tikukonzereni mwana wambuzi.”

16 Mngelo wa Yehova anayankha kuti, “Ngakhale mukundidikiritsa,
ine sindidya chakudya chanu. Koma ngati mukonze nsembe yopsereza
iperekeni kwa Yehova.” (Manowa n’kuti asakudziwa kuti munthuyo anali
mngelo wa Mulungu).

17 Tsono Manowa anapempha mngelo wa Yehova kuti, “Chonde tidzi-
witseni dzina lanu kuti zikadzachitika zimene mwanenazi ife tidzakule-
mekezeni?”

18 Iye anayankha kuti, “N’chifukwa chiyani mukufunsa dzina langa?
Dzina laketu ndi lodabwitsa.” 19 Ndipo Manowa anatenga mwana
wambuzi pamodzi ndi chopereka cha chakudya nakapereka nsembe pa
thanthwe kwa Yehova ndipo Yehova anachita zodabwitsa kwa Manowa
ndi mkazi wake akuona. 20 Pamene malawi a moto amakwera kumwamba
kuchoka pa guwa, mngelo wa Yehova uja anakwera kumwamba m’malawi
a motowo Manowa ndi mkazi wake akuona. Tsono anadzigwetsa pansi
naweramitsa mitu yawo pansi. 21 Mngelo wa Yehova uja sanaonekerenso
kwa Manowa ndi mkazi wake. Choncho Manowa anazindikira kuti anali
mngelo wa Yehova.

22 Iye anawuza mkazi wake kuti, “Ife tifa basi pakuti taona Mulungu!”

23 Koma mkazi wake anamuyankha kuti, “Yehova akanafuna ku-
tipha sakanayilandira nsembe yathu yopsereza ndi chopereka chathu

chachakudya chija, ndipo sakanationetsanso zinthu zonsezi kapena ku-
tiwuza zinthu ngati zimenezi nthawi ino."
24 Motero mkaziyo anabereka mwana wa mwamuna, namutcha dzina
lake Samsoni. Iye anakula ndipo Yehova anamudalitsa. 25 Mzimu wa
Yehova unayamba kumulimbikitsa pamene ankakhala ku misasa ya anthu
a fuko la Dani, malo amene anali pakati pa Zora ndi Esitaoli.

# 14

*Ukwati wa Samsoni*

1 Samsoni anapita ku Timna ndipo kumeneko anaonako mtsikana wa
Chifilisiti. 2 Atabwerera kwawo, anawuza abambo ndi amayi ake kuti, "Ine
ndaona mtsikana wa Chifilisiti ku Timna, tsono mukanditengere ameneyo
kuti akhale mkazi wanga."
3 Koma abambo ndi amayi ake anayankha kuti, "Kodi palibe mkazi
pakati pa abale akowa kapena pakati pa anthu a mtundu wako, kuti iwe
upite kukapeza mkazi kwa Afilisti anthu osachita mdulidwe?"
Koma Samsoni anawuza abambo ake kuti, "Kanditengereni ameneyu
basi, pakuti ndamukonda." 4 (Abambo ndi amayi ake sankadziwa kuti
zimenezi zinali zochokera kwa Yehova, pakuti Yehova amafuna powapez-
era chifukwa Afilistiwo. Nthawi imeneyo n'kuti Afilisti akulamulira
Aisraeli). 5 Choncho Samsoni pamodzi ndi abambo ake anapita ku
Timna. Akuyandikira minda ya mpesa ya ku Timna, mwadzidzidzi
anamva kubuma kwa mkango waung'ono ukubwera kumene kunali iye.
6 Tsono Mzimu wa Yehova unafika ndi mphamvu pa Samsoni ndipo
ngakhale analibe chida m'manja mwake, iye anakadzula mkangowo ngati
akukadzula mwana wambuzi. Koma sanawuze abambo kapena amayi
ake zimene anachitazo. 7 Kenaka Samsoni anapita kukakambirana ndi
mkaziyo, ndipo anamukonda mtsikanayo.
8 Patapita nthawi, Samsoni anabwerera kukatenga mtsikana uja. Panjira
anapatuka kukaona mkango unawupha uja, ndipo anangoona njuchi zili
mu mkangowo pamodzi ndi uchi wake. 9 Tsono anakomberako uchi uja
m'manja mwake ndi kumapita akudya. Atabwereranso kwa abambo ndi
amayi ake, anawapatsako uchiwo ndipo anadya. Koma sanawawuze kuti
uchi umenewo anawufula mu mkango wakufa.
10 Tsopano Samsoni anapita ku nyumba kwa mtsikanayo. Ndipo
kumeneko Samsoni anakonza phwando monga ankachitira anyamata.
11 Makolo a mkwatibwiyo atamuona, anasankha anyamata makumi atatu
kuti akhale naye.
12 Samsoni anawawuza kuti, "Bwanji ndikuphereni mwambi. Mukandi-
wuza tanthauzo lake asanathe masiku asanu ndi awiri aphwandowa,
ndidzakupatsani zovala makumi atatu za bafuta ndi zina makumi atatu
za tsiku la chikondwerero. 13 Koma ngati simutha kundiwuza tanthauzo
lake, inuyo mudzandipatsa zovala makumi atatu zabafuta ndi zina za tsiku
la chikondwerero."
Iwo anamuyankha kuti, "Tiwuze mwambi wakowo tiwumve."
14 Iye anati,
"Chakudya chinatuluka mu chinthu chodya chinzake;
ndipo chozuna chinatuluka mu chinthu champhamvu."
Panapita masiku atatu anthuwo akulephera kumasulira mwambiwo.
15 Tsiku lachinayi anthuwo anawuza mkazi wa Samsoni kuti, "Umun-
yengerere mwamuna wako kuti akuwuze tanthauzo la mwambiwu. Ngati

sutero tikutentha iweyo pamodzi ndi nyumba ya abambo ako. Kodi
unatiyitana kuti mudzatilande zinthu zathu?”
16 Kenaka mkazi wa Samsoni anayamba kulira pamaso pake namuwuza
kuti, “Inu mumandida ndipo simundikonda. Mwaphera anyamata a
mtundu wathu mwambi, koma ine wosandiwuza tanthauzo lake.”
Samsoni anamuyankha kuti, “Taona sindinawuze abambo kapena
amayi anga, ndiye ndiwuze iweyo?” 17 Mkaziyo anamulirira masiku onse
asanu ndi awiri aphwandowo. Choncho pa tsiku lachisanu ndi chiwiri
anamuwuza tanthauzo lake popeza amamukakamiza. Ndipo mkaziyo
anakawuza abale ake aja tanthauzo la mwambiwo.
18 Pambuyo pake anthu a mu mzinda aja anamuwuza Samsoni pa tsiku
lachisanu ndi chiwiri dzuwa lisanalowe kuti,
“Chozuna n’chiyani choposa uchi?
Champhamvu n’chiyani choposa mkango?”
Samsoni anawawuza kuti,
“Mukanapanda kutipula ndi ng’ombe yanga yaying’ono,
simukanatha kumasulira mwambi wangawu.”
19 Ndipo Mzimu wa Yehova unafika pa iye mwamphamvu. Choncho
anatsikira ku Asikeloni naphako anthu makumi atatu, natenga zovala
zawo za tsiku la chikondwerero napereka kwa anthu amene anamasulira
mwambi wake. Kenaka anabwerera ku nyumba ya abambo ake ndi
mkwiyo waukulu. 20 Ndipo mkazi wa Samsoniyo anamukwatitsa kwa
amene anali mnzake womuperekeza pa ukwati paja.

# 15

*Samsoni Abwezera Afilisti*

1 Patapita nthawi, mu nyengo yodula tirigu, Samsoni anatenga kamwana
kambuzi ndipo anapita kukacheza kwa mkazi wake. Iye anati, “Ndikufuna
kukalowa ku chipinda cha mkazi wanga.” Koma abambo a mkaziyo
anamuletsa kutero.
2 Abambo a mkaziyo anati, “Ine ndimaganiza kuti umamuda kwambiri
n’chifukwa chake ndinamupereka kwa mnzako. Kodi mng’ono wake
uja sindiye wokongola kupambana iye? Ingotengani ameneyo m’malo
mwake.”
3 Samsoni anawawuza kuti, “Pano sindikhala wochimwa ndikawachita
choyipa chachikulu Afilistiwa.” 4 Choncho Samsoni anapita nakagwira
nkhandwe 300 nazimangirira michira ziwiriziwiri ndipo pa fundo iliyonse
ya michirayo anamangirira nsakali. 5 Anayatsa nsakalizo kenaka ndi
kuzitayira nkhandwe zija m’minda ya tirigu ya Afilisti, ndipo zinatentha
milu ya tirigu, ndi wosadula yemwe pamodzi ndi mitengo ya mpesa ndi
ya olivi.
6 Tsono Afilisti anayamba kufunsana kuti, “Ndani wachita izi?” Ena
anati, “Ndi Samsoni mkamwini wa munthu wa ku Timna uja chifukwa
Mtimunayo anatenga mkazi wake ndi kumupereka kwa mnzake.”
Choncho Afilisti anapita kukatentha mtsikanayo pamodzi ndi abambo
ake. 7 Samsoni anawawuza kuti, “Ngati mumachita zangati zimenezi,
ndiye ine sindileka mpaka nditakulipsirani.” 8 Choncho Samsoni ana-
menyana nawo koopsa ndipo anapha ambiri a iwo. Kenaka anakalowa
m’phanga la Etamu, nakhala momwemo.
9 Pambuyo pake Afilisti anakamanga misasa ya nkhondo m’dziko la
Yuda, ndi kuthira nkhondo m’dera la Lehi. 10 Anthu a fuko la Yuda
anafunsa kuti, “N’chifukwa chiyani mwabwera kudzamenyana nafe?”

Iwo anayankha kuti, “Tabwera kudzamanga Samsoni ndi kuti timuchite zofanana ndi zimene anatichita.”

11 Ndipo anthu 3,000 a ku Yuda anapita ku phanga la Etamu, ndi kukamufunsa Samsoni kuti, “Kodi iwe sudziwa kuti ife amatilamulira ndi Afilisti? Tsono ndi chiyani chimene watichitachi?”

Iye anayankha kuti, “Ine ndinachita zomwe iwo anandichita.”

12 Iwo anati kwa iye, “Ife tabwera kuti tikumange ndi kukupereka kwa Afilisti.”

Ndipo Samsoni anati, “Lonjezani mwa lumbiro kuti simundipha ndinu.”

13 Iwo anamuyankha kuti, “Ayi, ife sitikupha. Koma tingokumanga ndi kukupereka m’manja mwa Afilisti.” Choncho anamumanga ndi
zingwe ziwiri zatsopano namutulutsa m’phanga muja. 14 Samsoni anafika
ku Lehi, ndipo Afilisti anamuchingamira akufuwula. Nthawi yomweyo Mzimu wa Yehova unatsika pa iye mwamphamvu ndipo zingwe zimene anamumanga nazo zinasanduka ngati thonje lopsa m’moto, zinachita
ngati zasungunuka n’kuchoka m’manja mwake. 15 Anapeza chibwano cha
bulu amene anali atangofa kumene. Anachitola ndi kuphera nacho anthu 1,000.

16 Ndipo Samsoni anati,
“Ndi chibwano cha bulu,
milu ndi milu ya anthu.
Ndi chibwano cha bulu,
ndapha anthu 1,000.”

17 Atatsiriza kuyankhula, anataya chibwanocho, ndipo malowo anawatcha Ramati-Lehi.

18 Pambuyo pake anamva ludzu kwambiri ndipo anayitana Yehova mopempha kuti, “Inu mwapatsa mtumiki wanu chipulumutso chachikulu chotere. Kodi tsopano ndife ndi ludzu ndi kugwidwa ndi anthu os-
achita mdulidwewa?” 19 Pamenepo Mulungu anang’amba nthaka ku
Lehi, ndipo madzi anatuluka m’dzenjemo. Samsoni anamwa madziwo, ndipo mphamvu zake zinabwerera nakhalanso monga analili. Choncho chitsimecho chinatchedwa Eni-Hakore, ndipo chilipobe ku Lehiko mpaka lero.

20 Samsoni anatsogolera Israeli pa nthawi ya Afilisti kwa zaka makumi awiri.

# 16

*Samsoni ndi Delila*

1 Tsiku lina Samsoni anapita ku Gaza. Kumeneko anaonako mkazi
wachiwerewere, ndipo analowa mu nyumba yake. 2 Anthu a ku Gaza
anawuzidwa kuti, “Samsoni ali kuno!” Choncho anthuwo anazungulira malowo, kumubisalira usiku wonse ku chipata cha mzindawo. Iwo anakhala chete usiku wonse namanena kuti, “Tidzamupha mmamawa.”

3 Koma Samsoni anangogonako mpaka pakati pa usiku. Kenaka pakati pa usiku anadzuka nagwira zitseko za chipata cha mzinda ndi maferemu ake awiri, ndipo anazizula zonse pamodzi ndi mpiringidzo wowme. Anazisenza pa mapewa pake napita nazo pamwamba pa phiri loyang’anana ndi Hebroni.

4 Pambuyo pake, Samsoni anayamba kukonda mtsikana wina wa ku
chigwa cha Soreki dzina lake Delila. 5 Olamulira Afilisti anapita kwa
mkaziyo ndipo anati, “Umunyengerere Samsoni kuti udziwe chinsinsi cha mphamvu zake zoopsazi, komanso ndi mmene ife tingamupambanire

kuti timumange ndi kumugonjetsa. Ukatero aliyense wa ife adzakupatsa
ndalama zasiliva 1,100."

6 Choncho Delila anati kwa Samsoni, "Inu tandiwuzani pamene pagona
mphamvu zanu zoopsazi ndi mmene anthu akhoza kukumangirani kuti
akugonjetseni."

7 Samsoni anamuyankha kuti, "Ngati wina atandimanga ndi zingwe
zisanu ndi ziwiri zatsopano zosawuma, ndidzafowoka ndi kusanduka
ngati munthu wina aliyense."

8 Tsono atsogoleri a Afilisti aja anapita kwa mkazi uja namupatsa zingwe
zisanu ndi ziwiri zatsopano zosawuma, ndipo mkaziyo anamanga nazo
Samsoni. 9 Nthawi imeneyo n'kuti mkazi uja atayika anthu omubisalira
m'chipinda. Tsono anati kwa mwamuna wake, "Amuna anga, Afilisti
aja afika!" Koma iye anangodula zingwe zija ngati mmene imadukira
nkhosi ya chingwe ikamapsa. Choncho chinsinsi cha mphamvu zake
sichinadziwike.

10 Kenaka Delila anati kwa Samsoni, "Inu mwandipusitsa ndi kundiwuza
zabodza. Chonde tandiwuzani mmene munthu angakumangireni."

11 Iye anati, "Ngati aliyense atandimanga ine ndi zingwe zatsopano
zimene sanazigwiritseko ntchito, ndidzasanduka wofowoka ndi kukhala
monga munthu wina aliyense."

12 Choncho Delila anatenga zingwe zatsopano namumanga nazo. Ke-
naka anati "Amuna anga, Afilisti aja afikanso!" Nthawi iyi n'kuti anthu
omubisalira aja ali m'chipinda cham'kati. Koma iye anadulanso zingwe
m'manja ake ngati akudula ulusi wa thonje.

13 Ndipo Delila anati kwa Samsoni, "Mpaka tsopano mwakhala mukundi-
pusitsa ndi kumandiwuza zabodza. Chonde, tandiwuzani mmene munthu
angakumangireni."

Iye anayankha kuti, "Ngati njombi zisanu ndi ziwiri za kumutu kwanga
utazilukira mu cholukira nsalu ndi kuchimanga molimbika ndi chikhomo,
ndidzasanduka wofowoka ndi kukhala wofanana ndi munthu wina
aliyense." 14 Choncho iye akugona, Delila analukira njombi za ku mutu
kwa Samsoni mu cholukira nsalu nachimanga molimba ndi chikhomo.

Pambuyo pake anati kwa Samsoni, "Amuna anga, Afilisti aja abwera!"
Tsono iye anadzuka ku tulo, nazula chikhomo chija ndipo njombi
zinachoka mu cholukira chija.

15 Tsono mkaziyo ananenanso kwa iye kuti, "Munganene bwanji kuti
mumandikonda pamene mtima wanu suli pa ine? Aka ndi kachitatu
mukundipusitsa ndipo simunandiwuze pamene pagona mphamvu zanu
zoopsazi." 16 Tsono popeza anamupanikiza ndi mawu ake tsiku ndi tsiku
ndi kumukakamiza, mtima wa Samsoni unatopa pafupi kufa.

17 Choncho anamuwuza mkaziyo zonse za mu mtima mwake nati "Lumo
silinapitepo pa mutu wanga chifukwa ndakhala ndili Mnaziri wopatulikira
Mulungu chibadwire. Ngati nditametedwa mphamvu zanga zidzandi-
chokera, ndidzasanduka wofowoka ndipo ndidzafanana ndi munthu wina
aliyense."

18 Delila ataona kuti wamuwuza zonse za mu mtima mwake anatumiza
uthenga kukayitana akuluakulu a Afilisti nati, "Bweraninso kamodzi kano
kokha popeza wandiwululira zonse za mu mtima mwake." Choncho
akuluakulu a Afilisti aja anabwera ndi ndalama za siliva m'manja mwawo.
19 Mkazi uja anagoneka Samsoni pa miyendo yake. Kenaka anayitana
munthu wina ndipo anadzameta Samsoni njombi zisanu ndi ziwiri zija

kumutu kwake. Pamenepo anayamba kufowoka, ndipo mphamvu zake
zinamuchokera.

20 Pambuyo pake mkaziyo anamuyitana kuti, “Amuna anga, Afilisti aja
abwera!”

Iye anadzuka kutuloko, naganiza kuti, “Ndituluka monga ndimachitira
nthawi zonse ndi kudzimasula.” Koma sanadziwe kuti Yehova wamuchok-
era.

21 Afilisti anamugwira ndipo anamukolowola maso. Kenaka anapita
naye ku Gaza atamumanga ndi maunyolo achitsulo. Kumeneko anakhala
wa pamphero mu ndende. 22 Pambuyo pake tsitsi la pa mutu wake, monga
linametedwa, linayambanso kumera.

### *Imfa ya Samsoni*

23 Tsono atsogoleri a Afilisti anasonkhana kuti adzapereke nsembe
yayikulu kwa Dagoni mulungu wawo ndi kukondwerera popeza anka-
nena kuti, “Mulungu wathu wapereka Samsoni mdani wathu m’manja
mwathu.”

24 Anthuwo atamuona Samsoni, anayamba kutamanda mulungu wawo
popeza ankanena kuti,

“Mulungu wathu wapereka mdani wathu
  m’manja mwathu,
ndiye amene anawononga dziko lathu,
  napha anthu athu ambirimbiri.”

25 Ali m’kati mosangalala, anthu aja amafuwula kuti, “Mutulutseni
Samsoniyo kuti adzatisangalatse.” Choncho anamutulutsadi Samsoni
m’ndende, ndipo anawasangalatsadi.

Ndipo anamuyimiritsa pakati pa mizati. 26 Pambuyo pake Samsoni
anawuza mnyamata amene anamugwira dzanja kuti, “Ndilole kuti
ndikhudze mizati imene yachirikiza nyumba yonseyi kuti ndiyitsamire.”
27 Nthawi imeneyi n’kuti nyumbayo ili yodzaza ndi anthu aamuna ndi
aakazi. Olamulira onse a Afilisti anali momwemo, ndipo pamwamba
pa nyumbayo panali anthu 3,000 aamuna ndi aakazi amene amaonerera
Samsoni akusewera. 28 Tsono Samsoni anapemphera kwa Yehova kuti,
“Inu Yehova Ambuye anga, ndikumbukireni. Chonde ndilimbitseni nthawi
yokha ino, inu Yehova, kuti ndiwabwezere Afilistiwa chifukwa cha maso
anga awiri.” 29 Choncho Samsoni anagwira mizati iwiri yapakati imene
inkachirikiza nyumbayo. Anayitsamira ndi mphamvu zake zonse, dzanja
lake lamanja ku mzati wina ndi dzanja lamanzere ku mzati winanso,
30 ndipo Samsoni anati, “Ndife nawo pamodzi!” Nthawi yomweyo
anakankha ndi mphamvu zake zonse ndipo mizati inagwera atsogoleri
a Afilisti ndi anthu onse anali m’menemo. Tsono chiwerengero cha anthu
amene Samsoni anapha pa nthawi ya imfa yake chinaposa cha iwo amene
anawapha akanali ndi moyo.

31 Kenaka abale ake ndi onse a pa banja la abambo ake anapita
kukamutenga. Ndipo anakamuyika pakati pa Zora ndi Esitaoli m’manda
a abambo ake, Manowa. Iye anatsogolera Israeli kwa zaka makumi awiri.

## 17

### *Mafuno a Mika*

1 Munthu wina dzina lake Mika wochokera ku dziko la mapiri la
Efereimu anawuza amayi ake kuti 2 “Ndinamva inu mukutemberera

munthu amene anaba ndalama zanu zasiliva 1,100. Ndalamazo zili ndi
ine, ndinatenga ndine.”
Pamenepo amayi akewo anati, “Yehova akudalitse mwana wanga!”
3 Choncho Mika anabweza ndalama 1,100 za siliva kwa amayi ake,
ndipo amayi akewo anati, “Ine ndapatulira Yehova ndalama za silivazi
kuti mwana wanga aseme fano ndi kulikuta ndi siliva. Ndiye tsopano
ndikubwezera ndalamazo.”
4 Tsono Mika atabweza ndalama zija kwa amayi ake, iwo anatengapo
ndalama za siliva 200 namupatsa mmisiri wosula siliva. Iye anakonza
fano, nasungunula siliva uja ndi kulikutira fano lija. Ndipo Mika anayika
fanolo m’nyumba mwake.
5 Mikayu anali ndi kachisi, ndipo anapanga efodi ndi mafano otchedwa
terafimu. Anapatula mwana wake mmodzi kuti akhale wansembe.
6 Masiku amenewo kunalibe mfumu ku Israeli. Aliyense amachita zomwe
zinamukomera.
7 Ku Betelehemu m’dziko la Yuda kunali mnyamata wina amene anali
wa fuko la Levi. 8 Iyeyu anachoka mu mzinda wa Betelehemu uja ku
Yuda kukafuna malo ena okhala. Akuyenda, anafika ku dziko la mapiri la
Efereimu ku nyumba ya Mika.
9 Tsono Mika anamufunsa kuti, “Mukuchokera kuti?”
Ndipo iye anayakha kuti, “Ndine Mlevi wochokera ku Betelehemu
m’dziko la Yuda. Ndikufunafuna malo okhala.”
10 Tsono Mika anati kwa iye, “Khalani ndi ine. Mukhale ngati mlangizi
wanga ndi wansembe, ndipo ine ndizikupatsani ndalama za siliva khumi
pa chaka komanso zovala ndi zakudya.” 11 Choncho Mleviyo anavomera
kuti azikhala naye, ndipo mnyamatayo anakhala ngati mmodzi mwa
ana ake aamuna. 12 Pambuyo pake Mika anapatula Mleviyo ndipo
mnyamatayu anakhala wansembe. Tsono ankakhala m’nyumba ya Mika.
13 Ndipo Mika anati, “Tsopano ndadziwa kuti Yehova adzandikomera
mtima chifukwa Mleviyu ndiye wakhala wansembe wanga.”

# 18

*Fuko la Dani Likhala ku Laisi*

1 Masiku amenewo munalibe mfumu mu Israeli.
Ndipo anthu a fuko la Dani amafunafuna malo okhalamo ngati cholowa
chawo, chifukwa kufikira nthawi imeneyo anali asanalandire cholowa
chawo pakati pa mafuko a Israeli. 2 Choncho fuko la Dani linatumiza
kuchokera ku mabanja awo onse anthu olimba mtima asanu. Anthuwa
anachokera ku Zora ndi ku Esitaoli ndipo anatumidwa kukazonda ndi
kuliyendera dzikolo. Anthu amenewa ankayimira fuko lonse la Dani.
Anthuwa anawawuza kuti, “Pitani mukazonde dzikolo.”
Anthuwa anafika ku dziko la mapiri la Efereimu ndi kupita ku nyumba
ya Mika komwe anakagona. 3 Ali ku nyumba ya Mika anazindikira
mawu a mnyamata, Mlevi uja. Choncho anapita kwa iye namufunsa
kuti, “Unabwera ndi ndani kuno? Nanga ukuchita chiyani ku malo ano?
Komanso n’chifukwa chiyani uli kuno?”
4 Iye anawawuza zimene Mika anamuchitira ndipo anati, “Iye
anandilemba ntchito ndipo ndine wansembe wake.”
5 Kenaka iwo anati kwa iye, “Chonde tifunsire kwa Mulungu kuti tidziwe
ngati ulendo wathuwu tiyende bwino.”

6 Wansembeyo anawayankha kuti, “Pitani mu mtendere, Yehova ali ndi
inu pa ulendo wanuwu.”

7 Choncho anthu asanuwo ananyamuka ndipo anafika ku Laisi, kumene
anaona kuti anthu ankakhala mwabata monga anthu a ku Sidoni. Anali
anthu opanda chowavuta ndiponso aphee. Tsono popeza m’dziko mwawo
analibe chosowa, iwo anali a chuma. Anaonanso kuti anthuwo ankakhala
kutali ndi Sidoni ndipo analibe ubale ndi wina aliyense.

8 Ozonda dziko aja atabwerera kwa abale awo ku Zora ndi Esitaoli, abale
awowo anawafunsa kuti, “Mwaonako zotani?”

9 “Tiyeni tikamenyane nawo nkhondo popeza taliona dziko lawolo kuti
ndi lachonde kwambiri. Kodi simuchitapo kanthu? Musachite mphwayi
kupita m’dzikomo ndi kukalilanda. 10 Mukalowa, mukapeza anthu amene
ali osatekeseka ndi dziko lalikulu. Yehova wakupatsani dziko limeneli.
Malowo ngosasowa kanthu kalikonse kopezeka pa dziko lapansi.”

11 Kenaka anthu 600 a fuko la Dani ananyamuka ku Zora ndi Esitaoli
atanyamula zida za nkhondo. 12 Tsono anakamanga msasa ku Kiriati-
Yearimu m’dziko la Yuda. Malowa ali kumadzulo kwa Kiriati-Yearimu.
Ichi ndi chifukwa chake malowo akutchedwa Mahane Dani mpaka lero.
13 Kuchokera kumeneko anapita ku dziko lamapiri la Efereimu ndipo
anafika ku nyumba ya Mika.

14 Anthu asanu amene anakazonda dziko la Laisi anati kwa abale awo,
“Kodi mukudziwa kuti imodzi mwa nyumba izi muli efodi, mafano a
m’nyumba otchedwa terafimu, fano losema ndiponso fano lokuta ndi
siliva? Ndiye mudziwe chochita.” 15 Choncho anthuwa anapatuka napita
ku nyumba ya Mika kumene mnyamata, Mlevi uja ankakhala ndipo
anamufunsa za mmene zinthu zilili. 16 Nthawi imeneyi n’kuti anthu 600 a
fuko la Dani aja atayima pa chipata atanyamula zida za nkhondo. 17 Anthu
asanu amene anakazonda dziko aja analowa ndi kukatenga fano losema,
efodi, fano la m’nyumba lotchedwa terafimu, ndi fano lokutidwa ndi siliva.
Nthawiyi n’kuti wansembe uja ndi anthu 600 okhala ndi zida za nkhondo
aja ali chiyimire pa chipata.

18 Anthuwo atalowa m’nyumba ya Mika ndi kutenga fano losema,
efodi, fano la m’nyumba, ndi fano lokutidwa ndi siliva, wansembeyo
anawafunsa kuti, “Kodi mukuchita chiyani?”

19 Iwo anamuyankha kuti, “Khala chete usayankhule. Tsagana nafe
ndipo udzakhala mlangizi wathu ndi wansembe wathu. Kodi si kwabwino
kwa iwe kukhala wansembe wa fuko lonse la Israeli m’malo mokhala
wansembe wa munthu mmodzi yekha?” 20 Wansembeyo anakondwera
ndipo anatenga efodi, fano la m’nyumba ndi fano losema natsagana
nawo. 21 Choncho iwo anatembenuka nachoka, atatsogoza ana, zoweta
ndi katundu wawo yense.

22 Atayenda mtunda pang’ono kuchokera pa nyumba ya Mika, anthu
amene amakhala pafupi ndi nyumba ya Mika anasonkhana kulondola
a fuko la Dani aja, ndipo anawapeza. 23 Atawafuwulira, a fuko la
Dani aja anachewuka ndipo anafunsa Mika kuti, “Chavuta n’chiyani kuti
usonkhanitse anthu chotere?”

24 Iye anayankha kuti, “Inu mwanditengera milungu imene ndinapanga
pamodzi ndi wansembe n’kumapita. Tsono ine ndatsala ndi chiyani?
Ndiye inu mungafunse kuti chavuta n’chiyani?”

25 Anthu a fuko la Dani aja anayankha kuti, “Usayankhuleponso kanthu
chifukwa anthu awa angapse mtima nakumenya ndipo iwe ndi banja

lako lonse n'kutayapo miyoyo yanu." 26 Choncho anthu a fuko la Dani
anapitiriza ulendo wawo. Mika ataona kuti anthuwo anali amphamvu
kuposa iye, anangotembenuka kubwerera kwawo.

27 Anthu a fuko la Dani aja anatenga zinthu zimene Mika anapanga
pamodzi ndi wansembe uja. Iwo anakafika ku Laisi kwa anthu a
phee, osatekeseka aja ndipo anawathira nkhondo, nawapha ndi kutentha
mzindawo ndi moto. 28 Panalibe wowapulumutsa chifukwa anali kutali
ndi Sidoni ndiponso sanali pa ubale ndi wina aliyense. Mzindawo unali
m'chigwa cha Beti-Rehobu.

Anthu a fuko la Adaniwo anawumanganso mzindawo ndi kumakha-
lamo. 29 Iwo anawutcha mzindawo Dani, kutengera dzina la kholo lawo
Dani, amene anali mwana wa Israeli, ngakhale kuti mzindawo poyamba
unali Laisi. 30 Anthu a fuko la Dani anayimiritsa fano losema lija.
Yonatani mwana wa Geresomu, mwana wa Mose pamodzi ndi ana ake
onse anakhala ansembe a fuko la Dani mpaka pa tsiku la ukapolo wa
dzikolo. 31 Choncho anthu a fuko la Dani ankapembedza fano limene Mika
anapanga nthawi yonse pamene nyumba ya Mulungu inali ku Silo.

# 19

*Mlevi ndi Mzikazi Wake*

1 Pa nthawi imeneyo ku Israeli kunalibe mfumu.

Mlevi wina ankakhala kutali ku dziko lamapiri la Efereimu. Iyeyu
anatenga mzikazi wa ku Betelehemu, m'dziko la Yuda. 2 Tsiku lina
mzikazi uja anakwiyira mwamuna wake ndipo anamuchokera kupita kwa
abambo ake ku Betelehemu m'dziko la Yuda. Anakakhala kumeneko
miyezi inayi. 3 Mwamuna wake anamulondola kuti akayankhule naye
mofatsa kumupempha kuti abwerere. Iye anali ndi antchito ake ndi abulu
ake awiri. Anafika ku nyumba kwa mkazi uja ndipo iye anamulowetsa
m'nyumba ya abambo ake. Abambo aja atamuona mnyamata uja
anamulandira mwachimwemwe. 4 Mpongozi wake, yemwe anali abambo
a mtsikanayo, anamupempha kuti aswere. Choncho anakhalako masiku
atatu. Ankadya, kumwa ndi kugona komweko.

5 Tsiku lachinayi anadzuka m'mamawa kukonzekera kuti azipita
kwawo, koma abambo ake a mtsikanayo anawuza mkamwini wawo
uja kuti, "Yambani mwadya chakudya, ndipo kenaka mutha kupita."
6 Choncho onse awiri anakhala pansi ndi kudya ndi kumwa pamodzi.
Atadya, abambo a mtsikanayo anati, "Chonde mugonenso konkuno mu-
sangalale." 7 Ndipo pamene mwamunayo anakonzeka kuti azipita, apon-
gozi ake anamuwumirizanso kuti asapite. Choncho anagona komweko
usiku umenewo. 8 Mmawa wa tsiku lachisanu, atadzuka kuti azipita
abambo ake a mtsikanayo anamuwuza kuti, "Yambani mwadya chakudya
ndipo mutandale mpaka madzulo." Choncho awiriwo anadya pamodzi.

9 Pambuyo pake munthu uja pamodzi ndi mzikazi wake ndiponso
mtumiki anakonzeka kuti azipita. Koma abambo a mtsikana uja anatinso
kwa iye, "Onani tsopano kukuda. Gonani konkuno pakuti tsiku latha kale.
Gonani ndipo musangalale. Mawa mudzuka m'mamawa ndi kumapita
kwanu." 10 Koma munthuyo sanafune kugonanso tsiku limenelo. Choncho
ananyamuka kumapita, ndipo anakafika ku malo oyang'anana ndi Yebusi
(ndiye kuti Yerusalemu). Iyeyo anali atatenga abulu ake awiri okhala ndi
zokhalira zake, ndipo mzikazi wake uja anali naye limodzi.

11 Akuyandikira ku Yebusi n'kuti kutada ndithu. Tsono mtumiki uja
anawuza mbuye wake kuti, "Tiyeni, tipatukire ku mzinda wa Ayebusiwa
ndipo tigone."

12 Mbuye wake anamuyankha kuti, "Ayi, tisapatukire ku mzinda wa
alendo, anthu amene sali Aisraeli. Koma tipitirire mpaka ku Gibeya."
13 Tsono anamuwuza mtumiki wake uja kuti, "Tiye tipite ku amodzi a malo
awa, ku Gibeya kapena ku Rama ndipo tikagone kumeneko." 14 Choncho
nayenda ulendo wawo, ndipo dzuwa linawalowera akuyandikira ku
Gibeya m'dziko la Benjamini. 15 Ndipo anapatukira kumeneko kuti
alowe mu mzinda wa Gibeya kukagona usiku umenewo. Anakalowa
mu mzindamo ndi kukakhala pabwalo popeza panalibe munthu amene
anawalandira ku nyumba kwake kuti akagone.

16 Pambuyo pake anangoona munthu wina wokalamba akuchokera ku
ntchito ya ku munda kwake madzulo. Iyeyu anali wa ku dziko la mapiri
ku Efereimu, koma ankakhala ku Gibeya. Koma anthu a kumeneko anali
a fuko la Benjamini. 17 Munthu wokalamba uja anakweza maso ndipo
anaona munthu wa paulendo uja atakhala pabwalo la mzindawo, ndipo
anamufunsa kuti, "Kodi mukupita kuti? Nanga mukuchokera kuti?"

18 Iye anayankha kuti, "Tikuchokera ku Betelehemu ku dziko la Yuda
ndipo tikupita kutali ku dziko lamapiri la Efereimu kumene ndimakhala.
Ndinapita ku Betelehemu m'dziko la Yuda ndipo tsopano ndikubwerera
kwathu. Koma palibe aliyense amene wanditengera ku nyumba yake.
19 Tili ndi udzu ndi chakudya cha abulu athu. Tilinso ndi buledi ndi vinyo
wokwanira ifeyo: ine, mdzakazi wanuyu, ndi mtumiki amene ali nafeyu.
Palibe chimene tikusowa."

20 Munthu wokalambayo anati, "Mtendere ukhale nanu. Ine
ndikuthandizani pa zosowa zanu zonse, koma musagone pabwalo usiku
uno." 21 Choncho anapita nawo ku nyumba yake, ndipo anawapatsa abulu
ake chakudya. Alendo aja anasamba mapazi awo, nalandira chakudya ndi
chakumwa.

22 Pamene ankadya mosangalala, anangoona anthu ena achabechabe
a mu mzindawo azungulira nyumba ija n'kumamenya chitseko. Tsono
anawuza mwini nyumbayo, munthu wokalamba uja kuti, "Mutulutse
munthu amene wabwera m'nyumba yakoyu kuti tigone naye."

23 Koma mwini nyumba uja anatuluka ku bwalo nawawuza kuti,
"Ayi, abale anga musachite zoyipa zotere. Popeza munthu uyu
walowa m'nyumba mwanga muno, musachite chinthu chonyansa chotere.
24 Onani, pano pali mwana wanga wamkazi wosadziwa mwamuna
pamodzi ndi mzikazi wa mlendoyu. Ndikutulutsirani amenewa tsopano
ndipo atengeni ndi kuchita nawo chomwe chikukomerani. Koma musa-
chite chinthu chonyansa ndi munthuyu."

25 Koma anthuwo sanafune kumumvera. Choncho mlendo uja anagwira
mzikazi wake namutulutsa kuja kumene kunali iwo. Tsono iwowo
anagona naye ndi kuchita naye zonyansa usiku wonse mpaka mmawa.
M'bandakucha anamulola kuti apite. 26 Ndipo mmawa kukucha mzikazi
uja anabwerera nakagwa pansi pa khomo pa nyumba imene mwamuna
wake anali, ndipo anakhala pomwepo mpaka kunayera.

27 Mwamuna wake anadzuka m'mamawa, natsekula chitseko cha
nyumba kuti atuluke ndi kumapita. Koma anangoona mzikazi wake uja
ali thapsa pa khomo la nyumbayo, manja ake ali pa khonde. 28 Iye
anati kwa mkaziyo, "Dzuka tizipita." Koma sanayankhe kanthu. Kenaka
anamukweza pa bulu wake ndipo ananyamuka kumapita kwawo.

29 Atafika ku nyumba yake, anatenga mpeni, nagwira mzikazi wake uja
ndi kuduladula thupi lake nthuli khumi ndi ziwiri. Kenaka anazitumiza
ku zigawo zonse za Israeli. 30 Aliyense amene anaona zimenezi ankanena
kuti, "Zoterezi sizinaonekepo kuyambira pamene Aisraeli anatuluka
m'dziko la Igupto mpaka lero lino. Ganizirani bwino chinthu chimenechi
ndipo tiwuzeni zoyenera kuchita!"

# 20

*Aisraeli Achita Nkhondo ndi Fuko la Benjamini*

1 Ndipo Aisraeli onse kuyambira ku dziko la Dani mpaka ku Beeriseba
ndiponso ku dziko la Giliyadi ananyamuka ngati munthu mmodzi naka-
sonkhana pamaso pa Yehova ku Mizipa. 2 Atsogoleri a anthu onse ndi
a mafuko onse Aisraeli anali nawo pa msonkhano wa anthu a Mulungu.
Onse pamodzi analipo asilikali oyenda pansi 400,000 atanyamula malu-
panga. 3 Anthu a fuko la Benjamini anali atamva kuti Aisraeli apita ku
Mizipa. Tsono Aisraeli anati, "Tiwuzeni, zinthu zoyipa izi zinachitika
bwanji."

4 Choncho Mlevi uja, mwamuna wa mkazi wophedwa uja anayankha
nati, "Ine ndinapita ku Gibeya m'dziko la Benjamini pamodzi ndi mzikazi
wanga kuti tikagone kumeneko. 5 Usiku anthu a ku Gibeya anandiwukira,
nazinga nyumba munali ine. Ankafuna kundipha ndipo anagona ndi
mzikazi wanga momukakamiza mpaka anafa. 6 Ine ndinatenga mzikazi
wangayo ndi kumudula nthulinthuli ndikuzitumiza kwa fuko lililonse
la Aisraeli. Anthu amenewa, zedi achita chinthu chonyansa kwambiri
m'dziko lino la Israeli. 7 Ndi zimenezotu inu Aisraeli nonse; yankhulaponi
mawu ndi kupereka maganizo anu."

8 Anthu onse anayimirira ngati munthu mmodzi nanena kuti, "Palibe
mmodzi wa ife amene apite ku nyumba kwake. Palibe amene abwerere
ku nyumba kwake. 9 Koma tsopano chimene ife tichite ndi dziko la
Gibeya ndi ichi: Tidzapita kukamenyana nawo potsatira zimene maere
anene. 10 M'mafuko onse a Aisraeli tidzasankha anthu khumi pa anthu
100 aliwonse: ndiye kuti anthu 100 pa anthu 1,000 aliwonse kapena
anthu 1,000 pa anthu 10,000 aliwonse. Anthu amenewa adzasonkhanitsa
zakudya za ankhondo, ndipo ankhondowo adzapita kukalipsira anthu a ku
Geba m'dziko la Benjamini chifukwa chochita chinthu chonyansa chotere
m'dziko la Israeli." 11 Choncho anthu a ku Israeli anasonkhana pamodzi
nagwirizana chimodzi, kukalimbana ndi mzindawo.

12 Mafuko a Israeli anatumiza anthu kwa fuko lonse la Benjamini
kukafunsa kuti, "Kodi zoyipa zachitika pakati panuzi ndi zotani? 13 Tsono
tikuti mutipatse anthu achabechabe a ku Gibeya kuti tiwaphe kuti tichotse
chinthu choyipachi m'dziko la Israeli."

Koma fuko la Benjamini silinafune kumvera zimene ananena Aisraeli
anzawo. 14 M'malo mwake, Abenjaminiwo anatuluka m'mizinda yawo
ku Gibeya kukamenyana ndi Aisraeli. 15 Tsiku limenelo Abenjamini ana-
sonkhanitsa kuchokera ku mizinda yawo ankhondo 26,000 amalupanga
awo, osawerengera anthu ena 700 a ku Gibeya amene anasankhidwa.
16 Mwa onsewa panali ankhondo 70 amanzere amene aliyense anali
wodziwa kulasa ngakhale tsitsi limodzi ndi mwala osaphonya.

17 Aisraeli, kupatula fuko la Benjamini, anasonkhanitsa anthu 400,000 a
malupanga, onse odziwa bwino nkhondo.

18 Ndipo Aisraeli ananyamuka kupita ku Beteli kukafunsira kwa Mu-
lungu. Iwo anati, “Ndani mwa ife amene angayambe kukamenyana ndi
fuko la Benjamini?”
Yehova anayankha kuti, “Fuko la Yuda ndilo liyambe.”
19 Mmawa mwake Israeli ananyamuka nakamanga msasa
moyang’anana ndi Gibeya. 20 Aisraeli anapita kukachita nkhondo ndi
fuko la Benjamini ndipo anandandalika ankhondo awo moyang’anana ndi
Gibeya. 21 A fuko la Benjamini anatuluka ku Gibeya ndipo tsiku limenelo
anapha Aisraeli 22,000 ku nkhondoko. 22 Koma ankhondo a Israeli
analimbikitsananso mtima ndipo anasonkhanitsanso kachiwiri ankhondo
awo pa malo pamene anawandandalika poyamba paja. 23 Aisraeli anapita
kukalira pamaso pa Yehova mpaka madzulo. Iwo anafunsa Yehova kuti,
“Kodi tipitenso kukamenyana ndi a fuko la Benjamini abale athu?”
Yehova anayankha kuti, “Pitani mukalimbane nawo.”
24 Ndipo Aisraeli anayandikiranso pafupi ndi fuko la Benjamini tsiku
lachiwiri lake kuti amenyane nawo. 25 Pa tsiku lachiwiri lomwelo Aben-
jamini anatulukanso mu mzinda wa Gibeya ndipo anaphanso ankhondo
18,000. Onse amene anawaphawo anali odziwa kugwiritsa ntchito bwino
malupanga.
26 Tsono Aisraeli onse, gulu lonse la ankhondo, anapita ku Beteli
kukalira pamaso pa Yehova. Anakhala pansi nasala zakudya tsiku lonse
mpaka madzulo. Anapereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano
pamaso pa Yehova. 27 Bokosi la Chipangano cha Yehova linali kumeneko.
28 Finehasi mwana wa Eliezara mwana wa Aaroni ndiye ankatumikira
nthawi imeneyo. Tsono Aisraeli anafunsa Yehova kuti, “Kodi tipitenso
kukachita nkhondo ndi m’bale athu Abenjamini, kapena ayi?”
Yehova anayankha kuti, “Pitaninso chifukwa mawa ndidzawapereka
m’manja mwanu.”
29 Choncho Aisraeli anayika anthu obisalira mozungulira Gibeya.
30 Tsiku lachitatu anapita kukamenyana ndi Benjamini ndipo anayika
ankhondo m’malo mwawo kuti amenyane ndi Gibeya monga anachitira
poyamba. 31 Abenjamini anatuluka kukamenyana nawo anthuwo ndipo
anapita kutali ndi mzindawo. Iwo anayamba kupha Aisraeli monga
poyamba paja, kotero kuti anapha anthu pafupifupi makumi atatu.
Mitembo ya ena inali mu misewu yayikulu yopita ku Beteli ndi ku Gibeya,
ndipo ina inali kwina poyera.
32 Abenjamini ankanena kuti, “Tikuwagonjetsa monga poyamba.” Koma
Aisraeli ankanena kuti, “Tiyeni tithawe kuti apite ku msewu chapatali ndi
mzinda wawo.”
33 Choncho Aisraeli onse anachoka m’malo mwawo ndi kukandanda ku
Baala-Tamara, ndipo Aisraeli obisalira aja anatuluka m’malo awo kum-
mawa kwa Geba. 34 Aisraeli osankhidwa 10,000 ndiwo anabwera kudza-
limbana ndi mzinda wa Gibeya. Nkhondoyo inafika poyipa kwambiri
mwakuti Abenjamini samadziwa kuti zoopsa zili pafupi kuwagwera.
35 Tsono Yehova anagonjetsa Abenjamini pamaso pa Israeli motero kuti
Aisraeli anapha ankhondo a Abenjamini 25,100 tsiku limenelo. 36 Choncho
Abenjamini anaona kuti agonjetsedwa.
Paja Aisraeli anathawa fuko la Benjamini chifukwa ankadalira anthu
amene anawayika kuti abisalire mzinda wa Gibeya. 37 Tsono anthu amene
anabisala aja anachita changu kuwuthira nkhondo mzinda wa Gibeyawo.
Ndipo anapha anthu onse a mu mzindawo ndi lupanga. 38 Chizindikiro

chimene Aisraeli anapangana ndi anthu obisalira aja chinali chakuti
obisalira aja akangofukiza utsi wambiri ngati mtambo mu mzindamo,
39 ndiye kuti Aisraeli enawo abwerere ku nkhondo.
Pa nthawiyo n'kuti Abenjamini atayamba kale kumenya Aisraeliwo
kwambiri ndi kupha pafupifupi anthu makumi atatu. Ndipo iwo ankanena
kuti, "Ndithu tawapha monga poyamba paja." 40 Koma pamene utsi
wa chizindikiro uja unayamba kukwera tolotolo mmwamba kuchoka
mu mzindamo, Abenjamini anayang'ana m'mbuyo ndipo anangoona utsi
mu mzinda onse uli tolotolo kukwera mmwamba. 41 Kenaka Aisraeli
anabwerera ndipo Abenjamini anachita mantha, chifukwa anaona kuti
zoopsa zili pafupi kuwagwera. 42 Choncho anathawa pamaso pa Aisraeli
kudzera njira ya ku chipululu, koma nkhondo inawapeza. Ndipo
anaphedwa kumeneko ndi Aisraeli amene anachokera mu mzindamo.
43 Anawazungulira Abenjaminiwo, nawathamangitsa ndi kuwagonjetser-
atu osawachitira chifundo mpaka ku dera la kummawa kwa Gibeya.
44 Abenjamini 18,000 olimba mtima anaphedwa. 45 Koma ena anatem-
benuka nathawira ku chipululu ku thanthwe la Rimoni. Mwa iwowa
Aisraeli anapha Abenjamini 5,000 m'misewu yayikulu. Anawapitikitsabe
Abenjaminiwo mpaka kufika ku Gidomu ndi kuphanso ena 2,000.
46 Pa tsiku limenelo Abenjamini olimba mtima okhala ndi malupanga
okwana 25,000 anafa. 47 Koma anthu 700 anabwerera ndi kuthawira
ku chipululu ku thanthwe la Rimoni kumene anakhalako miyezi inayi.
48 Aisraeli anabwerera kukamenyana ndi Abenjamini otsala ndi kuwapha
ndi lupanga kuphatikizapo ziweto ndi zonse anali nazo. Ndipo anayatsa
moto mizinda yonse anayipeza.

# 21

*Akazi a Abenjamini*

1 Aisraeli anali atalumbira ku Mizipa kuti, "Palibe mmodzi wa ife
adzapereke mwana wake wamkazi kuti akwatiwe ndi mwamuna wa fuko
la Benjamini."
2 Anthu anapita ku Beteli kumene anakakhala pansi pamaso pa Mulungu
mpaka madzulo. Iwo anakweza mawu nalira kwambiri. 3 Iwo ankanena
kuti, "Yehova Mulungu wa Israeli, n'chifukwa chiyani izi zachitika m'dziko
la Israeli kuti lero fuko limodzi lisowe mu Israeli?"
4 Mmawa mwake anthu anadzuka namanga guwa lansembe ndi ku-
pereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano.
5 Kenaka Aisraeli anafunsa kuti, "Kodi ndani pakati pa mafuko a
Israeli sanafike ku msonkhano wa Yehova?" Anatero chifukwa anachita
malumbiro aakulu okhudza munthu amene alephere kupita ku Mizipa ndi
kuti woteroyo ayenera kuphedwa.
6 Tsono Aisraeli anamva chisoni chifukwa cha abale awo, Aben-
jamini. Iwo anati, "Lero fuko limodzi lachotsedwa mu Israeli. 7 Kodi
tingawapezere bwanji anthu otsalawa akazi woti awakwatire? Paja
ife tinalumbira kwa Yehova kuti sitidzapereka ana anthu aakazi kuti
awakwatire. 8 Kenaka anafunsa kuti, 'Kodi mu fuko la Israeli ndani
amene sanabwere pamaso pa Yehova ku Mizipa?' " Tsono panapezeka kuti
panalibe ndi mmodzi yemwe wochokera ku Yabesi Giliyadi amene anapita
ku msonkhano ku misasa kuja. 9 Pamene anthu anawerengana anangoona
kuti anthu a ku Yabesi Giliyadi palibe.

[10] Choncho msonkhano unatumiza anthu ankhondo 12,000 ndi kuwala-
mula kuti, “Mukaphe anthu onse okhala ku Yabesi Giliyadi, kuphatikizapo
akazi ndi ana.” [11] Izi ndi zimene mukachite. “Mukaphe mwamuna
aliyense ndi mkazi aliyense amene anadziwapo mwamuna.” [12] Iwo
anapeza atsikana 400 pakati pa anthu okhala mu Yabesi Giliyadi amene
anali asanadziwepo mwamuna ndipo anabwera nawo ku misasa ku Silo
m’dziko la Kanaani.

[13] Kenaka msonkhano wonse unatumiza uthenga kwa Abenjamini
amene ankakhala ku thanthwe la Rimoni kuwawuza kuti nkhondo
yatha. [14] Choncho Abenjamini anabwera nthawi imeneyo ndipo Aisraeli
anawapatsa akazi a ku Yabesi Giliyadi amene sanaphedwe. Koma
sanapezeke owakwanira.

[15] Aisraeli anamvera chisoni Abenjamini, chifukwa Yehova anachita
ngati waligwerula dzino fuko la Israeli. [16] Choncho akuluakulu a
msonkhano anati, “Kodi tikawapezera kuti akazi anthu otsalirawa
kuti awakwatire popeza kuti akazi a fuko la Benjamini anaphedwa?”
[17] Iwo anati, “Abenjamini amene anapulumukawa ayenera kukhala
ndi zidzukulu, kuti mtundu wa Israeli usafafanizike. [18] Ife sitingathe
kuwapatsa ana anthu aakazi kuti akwatire. Paja tinalumbira kuti, ‘Akhale
wotembereredwa aliyense amene adzapereka mwana wake wamkazi kwa
mwamuna wa fuko la Benjamini kuti akwatire.’ [19] Ndipo anati, ‘Paja ku
Silo kuli chikondwerero cha chaka ndi chaka cholemekeza Yehova. Tsono
Silo ali kumpoto kwa Beteli, kummawa kwa msewu wochokera ku Beteli
kupita ku Sekemu, ndiponso kummwera kwa Lebona.’ ”

[20] Choncho anawalamulira Abenjamini aja kuti, “Pitani mukabisale
m’minda ya mpesa [21] ndipo mukakhale tcheru. Ana aakazi a ku Silo
akadzatulukira kudzavina nawo magule, pomwepo inu mutuluke minda
ya mpesa ndi kukawagwira aliyense wake ndi kupita nawo ku dziko
la Benjamini. [22] Ngati abambo awo kapena alongo awo adzabwera
kudzadandaula kwa ife, tidzawawuza kuti, ‘Chonde, tikomereni mtima
powalola kuti atenga ana anu aakaziwo popeza kuti ife sitinawapezere
akazi pomenya nkhondo. Inunso simunachite kuwapatsa. Mukanatero
ndiye mukanapalamula.’ ”

[23] Abenjamini anachitadi zimenezi. Mwa akazi amene ankavina aja
anagwirapo ena, malingana ndi chiwerengero chawo, nawatenga kuti
akhale akazi awo. Kenaka ananyamuka kubwerera ku dziko la kwawo,
nakamanganso mizinda yawo ndi kumakhalamo.

[24] Pambuyo pake Aisraeli anachoka kumeneko ndi kubwerera kwawo,
ku mafuko ndi ku mabanja awo, aliyense ku dera la cholowa chake.

[25] Masiku amenewo kunalibe mfumu ku Israeli. Aliyense ankangochita
zimene zomukomera yekha.

# Rute

*Naomi ndi Rute*

1 Mu nthawi imene oweruza ankalamulira Israeli, munali njala m'dziko,
ndipo munthu wina wa ku Betelehemu m'dziko la Yuda anapita pamodzi
ndi mkazi wake ndi ana ake aamuna awiri, kukakhala ku Mowabu kwa
nthawi yochepa. 2 Dzina la munthuyo linali Elimeleki, dzina la mkazi
wake linali Naomi, ndipo mayina a ana awo aamuna anali Maaloni ndi
Kiliyoni. Iwo anali Aefurati ochokera ku Betelehemu ku Yuda. Ndipo
anapita kukakhala ku Mowabu.

3 Kenaka Elimeleki, mwamuna wake wa Naomi anamwalira ndipo
Naomiyo anatsala ndi ana ake aamuna awiri aja.

4 Iwo anakwatira akazi a Chimowabu; wina dzina lake Oripa ndi wina
Rute. Atakhala kumeneko pafupifupi zaka khumi, 5 Maloni ndi Kiliyoni
anamwaliranso kotero kuti Naomi anatsala yekha wopanda ana ake awiri
aja ndi mwamuna wake.

6 Naomi ndi apongozi ake awiri aja ananyamuka kubwerera kwawo
kuchokera ku Mowabu popeza anali atamva ali ku Mowabuko kuti Yehova
anakomera mtima anthu ake ndi kuwapatsa chakudya.

7 Naomi pamodzi ndi apongozi ake awiri aja anachoka kumene
ankakhala ndi kuyamba ulendo obwerera kwawo ku Yuda.

8 Kenaka Naomi anati kwa apongozi ake awiri aja, "Bwererani, aliyense
kwa amayi ake. Yehova akukomereni mtima, monga munachita ndi
malemu aja ndi ine ndemwe.

9 "Yehova akuthandizeni kuti aliyense wa inu apeze pokhala pabwino
komanso mwamuna." Kenaka anawapsompsona koma awiriwo analira
mokweza.

10 Ndipo anati kwa Naomi, "Ife tipita nawo kwa anthu akwanu."

11 Koma Naomi anati, "Bwererani kwanu ana anga. Chifukwa chiyani
mukufuna kupita ndi ine? Kodi ine ndingaberekenso ana ena kuti
akhale amuna anu? 12 Bwererani kwanu ana anga muzipita kwanu.
Ine ndakalamba kwambiri kotero kuti sindingakwatiwenso. Ngakhale
ndikananena kuti ndili nacho chikhulupiriro, ngakhale ndikanakhala
ndi mwamuna usiku uno, ndipo n'kubala ana aamuna, 13 kodi inu
mukanadikira kuti akule? Kodi mukanakhalabe osakwatiwa kudikira
iwowo? Ayi ana anga. Zimenezi zikundiwawa kwambiri kuposa inu,
chifukwa ndi ineyo amene Yehova wafuna kuti ndizunzike."

14 Atamva zimenezi analiranso kwambiri, ndipo Oripa anapsompsona
apongozi ake nawatsanzika, koma Rute anakakamirabe.

15 Naomi anati "Taona, m'bale wako wabwerera kwawo kwa anthu ake
ndi kwa milungu yake. Bwerera nawenso umulondole m'bale wako."

16 Koma Rute anayankha kuti, "Musandikakamize kuti ndikusiyeni
kapena kuti ndibwerere osakutsatani. Kumene inu mupite ine ndipita
komweko, ndipo kumene mukakhale inenso ndikakhala komweko. Abale
anu adzakhala abale anga ndipo Mulungu wanu adzakhala Mulungu
wanga. 17 Kumene mukafere inenso ndidzafera komweko ndipo komweko
ndikayikidwa m'manda. Yehova andichite choyipa chingakule motani,
ngati china chingatirekanitse ife kupatula imfa."

18 Naomi atazindikira kuti Rute watsimikiza kupita naye, analeka
kumukakamiza.
19 Choncho amayi awiriwo anapitiriza ulendo wawo mpaka anakafika
ku Betelehemu. Pamene ankafika mu Betelehemu, anthu onse a
m'mudzimo anatekeseka chifukwa cha iwowo ndipo amayi ambiri anka-
nena kuti, “Kodi uyu n'kukhala Naomi?”
20 Iye anawawuza kuti, “Musanditchenso Naomi. Muzinditchula ine
kuti Mara, chifukwa Wamphamvuzonse wandizunza kwambiri. 21 Ine nd-
inapita wolemera, koma Yehova wabwera nane wopanda kanthu. Nanga
munditchulirenji Naomi pamene Yehova wandisautsa. Wamphamvuzonse
uja wandigwetsera mavuto owawa.”
22 Naomi anabwerera kuchoka ku dziko la Mowabu pamodzi ndi Rute
mpongozi wake. Ndipo anafika ku Betelehemu nthawi yoyamba kukolola
barele.

# 2

*Rute Akumana ndi Bowazi*

1 Naomi anali ndi m'bale wake wolemera kwambiri wochokera ku banja
la mwamuna wake Elimeleki, dzina lake Bowazi.
2 Tsiku lina Rute, Mmowabu uja anati kwa Naomi, “Mundilole kuti
ndikakunkhe barele ku munda wa munthu aliyense amene akandikomere
mtima.” Naomi anati kwa iye, “Pita mwana wanga.”
3 Choncho Rute ananyamuka kupita kukakunkha ku minda yokololedwa
kale. Tsono zinangochitika kuti Rute anafika m'munda wa Bowazi, yemwe
anali wochokera ku banja la Elimeleki.
4 Posakhalitsa Bowazi anafika kuchokera ku Betelehemu ndipo analon-
jera okolola aja kuti, “Yehova akhale nanu!”
Iwo anayankha kuti, “Yehova akudalitseni.”
5 Bowazi anafunsa kapitawo wake amene ankayang'anira okolola aja
kuti, “Mayi uyo ndi ndani?”
6 Kapitawo uja anayankha kuti, “Mayiyu ndi Mmowabu amene anabw-
era ndi Naomi kuchokera ku dziko la Mowabu. 7 Iye anandipempha kuti,
‘Chonde mundilole kuti ndikunkhe barele m'minda moti akololamo kale.’
Iye wakhala akukunkha kuyambira mmawa mpaka tsopano lino osapuma
n'pang'ono pomwe.”
8 Choncho Bowazi anati kwa Rute, “Tamvera mwana wanga, usapite
kukakunkha m'munda wina, ndipo usachoke m'munda uno. Koma uzit-
sata adzakazi angawa. 9 Uziyang'ana munda akukolola anyamatawo aka-
makolola m'mundamu, ndipo iwe uzitsata pambuyo pawo. Ndawawuza
anyamatawo kuti asakuvutitse. Ndipo ukamva ludzu, uzipita ku mitsuko
ndi kukamwa madzi amene anyamatawa atunga.”
10 Atamva zimenezi Rute anawerama nazolikitsa nkhope yake pansi.
Kenaka anafunsa kuti, “Mwandikomera mtima chotere mlendo ngati ine
chifukwa chiyani?”
11 Bowazi anayankha kuti, “Ine ndawuzidwa zonse zimene wakhala
ukuchitira apongozi ako chimwalirire mwamuna wako. Ndamvanso
kuti unasiya abambo ndi amayi ako komanso dziko la kwanu ndi
kubwera kudzakhala ndi anthu amene sumawadziwa ndi kale lonse.
12 Yehova akubwezere pa zimene wachitazi. Yehova Mulungu wa Israeli,
amene wabwera pansi pa mapiko ake kuti akuteteze, akupatse mphotho
yayikulu.”

13 Rute anati, “Mwandikomera mtima, mbuye wanga. Ndipo mwan-
disangalatsa ndi kundiyankhula mwa chifundo ngakhale sindili mmodzi
mwa adzakazi anu.”
14 Nthawi ya chakudya cha masana Bowazi anati kwa iye, “Bwera
kuno, utenge buledi ndi kusunsa nthongo mu vinyo.” Choncho anakhala
pansi pafupi ndi okololawo, ndipo Bowazi anamupatsa chakudya ndi
nyama yowotcha. Anadya chilichonse amafuna ndipo chakudya china
chinatsalako.
15 Atanyamuka kuti azikakunkha, Bowazi analangiza anyamata ake
kuti, “Ngakhale mayiyu azikunkha pakati pa mitolo musamuletse ndi
kumuchititsa manyazi. 16 Koma muzimusololerako ngala zina za m’mitolo
ndi kumusiyira kuti azikunkha ndipo musamukalipire.”
17 Choncho Rute anakunkha m’mundamo mpaka madzulo. Kenaka ana-
puntha barele anakunkhayo, ndipo anakwanira pafupifupi makilogalamu
khumi.
18 Anasenza barele uja kupita naye ku mudzi, nakaonetsa apongozi
ake. Kenaka anatulutsa chakudya chimene chinatsalira atakhuta chija ndi
kupatsa apongozi ake.
19 Apongozi akewo anamufunsa kuti, “Kodi lero unakakunkha kuti?
Unakagwira kuti ntchitoyi? Adalitsike munthu amene anakukomera
mtimayo.” Ndipo Rute anawuza mpongozi wake za munthu amene ku
malo ake anakagwirako ntchito. Iye anati, “Munthuyo dzina lake ndi
Bowazi.”
20 Naomi anati kwa mpongozi wakeyo, “Munthu ameneyu amudalitse
Yehova, amene sanasiye kuchitira chifundo anthu amoyo ndi akufa omwe.
Anatinso munthu ameneyu ndi mnansi wapaphata. Ndiye ali ndi udindo
wotisamalira.”
21 Choncho Rute Mmowabuyo anati, “Iye anandiwuzanso kuti, ‘Uzitsata
antchito angawa mpaka atamaliza kukolola munda wonse.’ ”
22 Naomi anati kwa Rute mpongozi wake, “Kuli bwino mwana wanga
kuti uzipita ndi adzakazi ake kuopa kuti m’munda wa munthu wina
angakuvute.”
23 Choncho Rute ankatsatira adzakazi a Bowazi namakunkha mpaka
anthu atamaliza kudula barele ndi tirigu. Ndipo amakhalabe ndi
mpongozi wakeyo.

# 3

### *Rute ndi Bowazi ku Malo Wopunthira Tirigu ndi Barele*

1 Tsiku lina Naomi anafunsa mpongozi wake Rute kuti, “Mwana wanga,
kodi si kwabwino kuti ndikupezere kokhala kuti zinthu zizikuyendera
bwino? 2 Bowazi amene adzakazi ake wakhala nawo nthawi yonseyi,
si wachibale wathu kodi? Usiku uno akhala akupeta barele ku malo
opunthira. 3 Samba ndi kudzola mafuta onunkhira, ndipo uvale zovala
zako zabwino kwambiri. Kenaka upite ku malo opunthirako tirigu ndi
barele koma munthuyo asakakuzindikire kufikira atamaliza kudya ndi
kumwa. 4 Akamakagona, iwe ukaonetsetse malo amene wagonawo.
Kenaka upite ndi kuvundukula chofunda ku mapazi ake ndi kugona. Iyeyo
akakuwuza zoti uchite.”
5 Rute anayankha kuti, “Ndichita zonse zimene mwanena.”
6 Choncho Rute anapita ku malo opunthirawo ndipo anachita monga
momwe apongozi ake anamuwuza.

7 Atamaliza kudya ndi kumwa, Bowazi anakhala wosangalala, ndipo
anakagona pa mbali pa mulu wa barele. Tsono Rute anapita mwa
kachetechete, navundukula chofunda ku mapazi ake ndi kugona.
8 Tsono pakati pa usiku Bowazi anadzidzimuka, natembenuka, ndipo
anangoona mkazi akugona ku mapazi ake.
9 Iye anafunsa kuti, “Ndiwe yani?” Ndipo anayankha kuti, “Ndine
mdzakazi wanu Rute. Popeza ndinu wachibale amene muyenera kundi-
wombola, ndiye mundilowe chokolo.”
10 Ndipo Bowazi anati, “Mwana wanga, Yehova akudalitse popeza
kukoma mtima kumene wasonyeza panoku kwaposa koyamba kaja. Iwe
sunathamangire anyamata olemera kapena osauka. 11 Ndipo tsopano
mwana wanga usaope. Ine ndidzakuchitira chilichonse udzapemphe
popeza anzanga onse am'mudzi muno akudziwa kuti ndiwe mkazi
wa khalidwe labwino. 12 Ngakhale kuti ndinedi wachibale woyenera
kukusamala, koma alipo wachibale weniweni kuposa ine. 13 Gona
konkuno usiku uno mpaka mmawa. Tsono ngati iyeyu adzakulowa
chokolo, chabwino alowe. Koma ngati safuna kutero, ine ndikulumbira
pamaso pa Yehova Wamoyo kuti ndidzakulowa chokolo. Ugone kuno
mpaka mmawa.”
14 Choncho Rute anagona ku mapazi ake mpaka mmawa, koma
anadzuka mmamawa kusanayere chifukwa Bowazi anati, “Aliyense
asadziwe kuti kopondera barele kunabwera mkazi.”
15 Bowazi anati kwa Rute, “Bwera nacho kuno chofunda wavalacho
ndipo uchiyale pansi.” Ndipo atayala, Bowazi anathira makilogalamu
makumi awiri a barele ndi kumusenzetsa Rute. Rute anapita nakalowa
mu mzinda.
16 Rute atafika kwa apongozi ake anamufunsa kuti, “Zinayenda bwanji
mwana wanga?” Kenaka iye anafotokoza zonse zimene Bowazi anamu-
chitira.
17 Ndipo anati, “Munthuyo anandipatsa makilogalamu makumi awiri
awa a barele, nandiwuza kuti usapite kwa apongozi ako wopanda kanthu.”
18 Kenaka Naomi anati, “Mwana wanga, dikira mpaka titaona mmene
zinthu zikhalire chifukwa munthuyu salekera pomwepo, mpaka zinthuzi
zitakonzeka lero.”

# 4

*Bowazi Akwatira Rute*

1 Nthawi yomweyo Bowazi anapita ku chipata cha mzinda ndi kukhala
pansi kumeneko pabwalo losonkhanira. Tsono anangoona wachibale
woyenera kulowa chokolo uja akufika. Ndipo Bowazi anati, “Patukirani
kuno, bwenzi langa. Mubwere mudzakhale apa.” Choncho anapatuka
nakakhala pansi.
2 Bowazi anayitananso akuluakulu khumi a mu mzindamo nati, “Dza-
khaleni pansi apa,” ndipo anadzakhala pansi.
3 Kenaka anamuwuza oyenera kulowa chokolo uja kuti, “Naomi amene
wabwera kuchoka ku Mowabu akugulitsa malo amene anali a malemu
Elimeleki, m'bale wathu uja. 4 Choncho ndinaganiza zokuwuza zimenezi
kuti ugule mundawu pamaso pa anthu amene ali panowa, ndi pamaso pa
akuluakulu mwa abale athu. Ngati ukufuna kuwuwombola, uwombole.
Koma ngati sukufuna, undiwuze kuti ndidziwe, pakuti palibe wina
angawuwombole koma iweyo, ndipo pambuyo pa iwe pali ine.” Iye anati,
“Ine ndidzawuwombola.”

5 Tsono Bowazi anati, “Tsiku limene ukagule mundawo kwa Naomi,
udzatenganso Rute Mmowabu, mkazi wamasiye uja, kuti dzina la malemu
lisungike pa cholowa chake.”
6 Pamenepo wachibaleyo anati, “Sindingathe kuwuwombola mundawu
kuti ukhale wanga, kuopa kuti kutaya cholowa changa. Mugule ndinu. Ine
sindingathe.”
7 (Kale mu Israeli zinkatere ngati munthu afuna kuwombola kanthu
kapena kusinthana kanthu ndi mnzake kuti chikhale chakechake. Iye
ankavula nsapato imodzi namupatsa mnzakeyo. Imeneyo ndiyo inali njira
yochitira umboni mu Israeli).
8 Choncho wachibale uja atawuza Bowazi kuti, “Gulani ndinu
mundawu.” Iye anavula nsapato yake namupatsa Bowazi.
9 Ndipo Bowazi anawuza akuluakuluwo ndi anthu onse aja kuti,
“Nonsenu ndinu mboni lero, kuti ine ndagula kwa Naomi zonse zimene
zinali za malemu Elimeleki, zonse zimene zinali za malemu Kiliyoni
ndiponso za malemu Maloni. 10 Ndatenganso Rute Mmowabu uja mkazi
wa malemu Maloni, kuti akhale mkazi wanga, kuti dzina la malemu
Maloni lisungike pa cholowa chake, ndipo lisafafanizike pakati pa abale
ake ngakhalenso m’mudzi mwake. Nonsenu ndinu mboni lero lino.”
11 Ndipo akuluakulu aja ndi anthu onse amene anali pa chipata anati,
“Ife ndife mboni, ndipo Yehova amusandutsa mkazi amene akudzalowa
m’nyumba yakoyu kuti akhale ngati Rakele ndi Leya, amene anamanga
banja la Israeli. Ukhale munthu wosasowa kanthu mu Efurata ndi
munthu wotchuka mu Betelehemu. 12 Ana amene Yehova adzakupatsa
mwa mkaziyu adzamange banja lako kukhala la Perezi, amene Tamara
anamubalira Yuda.”

*Makolo a Davide*

13 Choncho Bowazi anakwatira Rute. Yehova anamudalitsa nakhala ndi
pakati, ndipo anabereka mwana wamwamuna.
14 Ndipo amayi osiyanasiyana anati kwa Naomi. “Alemekezeke Yehova,
amene lero lino sanakusiyeni nokha wopanda wachibale. Mwanayu
dzina lake likhale lotchuka mu Israeli. 15 Mwanayo adzakupatseni moyo
watsopano ndi kukuthandizani pa ukalamba wanu. Inde, mpongozi wanu
amene amakukondani, amenenso waonetsa kuti ali wopambana kwa inu
kuposa ana aamuna asanu ndi awiri, ndiye wakubalirani mwanayu.”
16 Kenaka Naomi anatenga mwanayo namufukata ndipo anakhala mlezi.
17 Amayi achinansi ake anati, “Naomi ali ndi mwana wamwamuna.”
Ndipo anamutcha dzina lake Obedi. Iye anali abambo a Yese abambo ake
a Davide.
18 Izi tsono ndizo zidzukulu za Perezi:

Perezi anali abambo a Hezironi.
19 Hezironi anali abambo a Ramu,
Ramu anali abambo a Aminadabu,
20 Aminadabu abambo a Naasoni,
Naasoni anali abambo a Salimoni,
21 Salimoni abambo a Bowazi,
Bowazi abambo a Obedi.
22 Obedi anali abambo a Yese,
ndipo Yese anali abambo a Davide.

# 1 Samueli

*Banja la Elikana*

1 Panali munthu wina wochokera ku Ramataimu, Mzofimu wa ku dziko
la mapiri la Efereimu. Iyeyu dzina lake anali Elikana ndipo anali mwana
wa Yerohamu, mwana wa Elihu, mwana wa Tohu, mwana wa Zufu wa
fuko la Efereimu. 2 Iye anali ndi akazi awiri, Hana ndi Penina. Penina
anali ndi ana, koma Hana analibe.
3 Chaka ndi chaka Elikana ankachoka ku mudzi kwawo kupita ku Silo
kukapembedza ndi kukapereka nsembe kwa Yehova Wamphamvuzonse.
Ku Siloko kunali ana awiri a Eli, Hofini ndi Finehasi amene anali
ansembe a Yehova. 4 Tsiku lopereka nsembe likafika Elikana amapereka
magawo a nsembeyo kwa mkazi wake Penina ndi kwa ana ake onse
aamuna ndi aakazi. 5 Ngakhale ankamukonda Hana, koma ankamupatsa
gawo limodzi popeza Yehova sanamupatse ana. 6 Tsono popeza Yehova
sanamupatse Hana ana, mkazi mnzakeyo ankamuyamba dala ndi cholinga
chomukwiyitsa. 7 Izi zimachitika chaka ndi chaka. Hana ankati
akamapita ku Nyumba ya Yehova mkazi mnzakeyo ankamunyogodola.
Choncho Hana ankangokhalira kulira osafuna ndi kudya komwe. 8 Tsono
mwamuna wake Elikana ankamufunsa kuti, "Hana ukulira chifukwa
chiyani? Wakhumudwa ndi chiyani kuti sukufuna ndi kudya komwe?
Kodi ine kwa iwe sindili woposa ana aamuna khumi?"
9 Tsiku lina atatha kudya ndi kumwa ku Silo kuja, Hana anayimirira
kukapemphera. Nthawiyi n'kuti wansembe Eli atakhala pa mpando pa
khomo la Nyumba ya Yehova. 10 Hana anavutika m'moyo mwake, ndipo
anapemphera kwa Yehova akulira kwambiri. 11 Ndipo iye analumbira kuti,
"Inu Yehova Wamphamvuzonse, ngati muyang'ana kusauka kwa mtumiki
wanune, ndi kuyankha pemphero langa osandiyiwala ine mtumiki wanu
pondipatsa mwana wamwamuna, ine ndidzamupereka mwanayo kwa inu
Yehova masiku onse a moyo wake. Lumo silidzapita pa mutu pake."
12 Akupemphera choncho kwa Yehova, Eli ankamuyang'ana pakamwa.
13 Hana ankapemphera chamumtima ndipo milomo yake inkangogwedera
koma mawu ake samamveka. Choncho Eli anaganiza kuti anali ataledzera.
14 Ndipo anamufunsa Hana kuti, "Kodi mukhala chiledzerere mpaka liti?
Pitani, ayambe wakuchokani vinyo mwamwayo."
15 Koma Hana anayankha kuti, "Sichoncho mbuye wanga. Ndakhala
ndikumukhuthulira Yehova chisoni changa. Sindinamwe vinyo
kapena chakumwa choledzeretsa chilichonse, popeza nthawi yonseyi
ndakhala ndikupereka kwa Yehova nkhawa yayikulu ndi mavuto anga.
16 Musaganize kuti mtumiki wanu ndi kukhala mkazi wachabechabe. Ine
ndakhala ndi kupereka nkhawa yanga yayikulu ndi zowawa zanga."
17 Eli anayankha, "Pitani mu mtendere, ndipo Mulungu wa Israeli
akupatseni zimene mwamupemphazo."
18 Hana anati, "Mundikomerebe mtima mtumiki wanune." Kenaka
anachoka nakadya, ndipo sanaonekenso wachisoni.
19 Elikana ndi banja lake anadzuka mmawa mwake nakapemphera
pamaso pa Yehova. Pambuyo pake anabwerera kwawo ku Rama.
Elikana anakhala pamodzi ndi mkazi wake, ndipo Yehova anamukumbuka
Hanayo. 20 Motero Hana anakhala ndi pakati ndipo anabereka mwana

wamwamuna. Anamutcha dzina lake Samueli, popeza anati, “Ndinachita kumupempha kwa Yehova.”

### *Hana Apereka Samueli kwa Yehova*

21 Elikana ndi banja lake lonse anapita kukapereka nsembe ya pa chaka
kwa Yehova ndi kukakwaniritsa malonjezo ake. 22 Koma Hana sanapite
nawo popeza anawuza mwamuna wake kuti, “Mwanayu akadzaleka kuyamwa, ndidzapita naye ndi kukamupereka pamaso pa Yehova ndipo adzakhala kumeneko moyo wake wonse.”
23 Elikana mwamuna wake anamuwuza kuti, “Chita chimene chakukomera. Tsala kuno mpaka utamusiyitsa kuyamwa, Yehova yekha akwaniritse mawu ake.” Choncho mkaziyo anatsala ku nyumba ndi kusamalira mwana wake mpaka atamuletsa kuyamwa.
24 Atamuletsa kuyamwa, Hana anatenga mwanayo ali wachichepere, ndikupita naye ku nyumba ya Yehova ku Silo. Anatenga ng’ombe yamphongo ya zaka zitatu, ufa wa makilogalamu khumi, ndi thumba
lachikopa la vinyo. 25 Tsono anapha ng’ombe yamphongo ija ndi kupereka
mwana uja kwa Eli. 26 Ndipo Hana anati kwa Eli, “Mbuye wanga,
ine ndikunenetsadi pamaso panu kuti ndine mkazi uja amene anayima
pamaso panu ndi kumapemphera kwa Yehova. 27 Ndinapempha mwana
uyu, ndipo Yehova wandipatsa chimene ndinamupempha. 28 Ndiye
tsopano ine ndikumupereka kwa Yehova. Pa moyo wake wonse adzakhala wa Yehova.” Ndipo onse anapembedza Yehova kumeneko.

## 2

### *Pemphero la Hana*

1 Ndipo Hana anapemphera nati,
“Moyo wanga ukukondwera mwa Yehova;
Ndiyenda mwa tukumutukumu chifukwa cha Yehova.
Pakamwa panga pakula ndi kuseka adani anga mowanyogodola.
Ndikukondwa chifukwa mwandipulumutsa.

2 “Palibe wina woyera ngati Yehova,
palibe wina koma inu nokha,
palibe thanthwe lofanana ndi Mulungu wathu.

3 “Musandiyankhulenso modzitama,
pakamwa panu pasatuluke zonyada,
pakuti Yehova ndi Mulungu wanzeru,
ndipo ndiye amene amayesa ntchito za anthu onse.

4 “Mauta a anthu ankhondo athyoka
koma anthu ofowoka avala dzilimbe.
5 Amene kale anali okhuta tsopano akukagula chakudya,
koma iwo amene anali ndi njala sakumvanso njala.
Amene anali wosabereka, wabereka ana aamuna asanu ndi awiri,
koma iye wobereka ana ambiri watsala yekha.

6 “Yehova amabweretsa imfa ndipo amaperekanso moyo,
amatsitsira ku manda ndipo amawatulutsakonso.
7 Yehova amasaukitsa ndipo amalemeretsa,
amatsitsa ndipo amakweza.

8 Iye amakweza osauka kuwachotsa pa fumbi,
ndipo amachotsa anthu osowa pa dzala.
Iye amawakhazika pamodzi ndi ana a mafumu,
amawapatsa mpando waulemu.

“Pakuti nsanamira za dziko lapansi ndi za Yehova,
anakhazika dziko lapansi pa nsanamirazo.
9 Iye adzateteza moyo wa anthu okhulupirika
koma anthu oyipa adzawonongedwa mu mdima.

“Pakuti munthu sapambana ndi mphamvu zake.
10 Yehova adzaphwanya omutsutsa.
Adzawaopsa ndi bingu kuchokera kumwamba;
Yehova adzaweruza mathero a dziko lapansi.

“Koma adzapereka mphamvu kwa mfumu yake,
adzakuza mphamvu za odzozedwa wake.”

11 Tsono Elikana anapita ku mudzi kwawo ku Rama, koma mnyamatayo amatumikira Yehova pansi pa ulamuliro wa wansembe Eli.

*Kuyipa kwa Ana a Eli*

12 Ana a Eli anali ana achabechabe pakuti samasamala za Yehova.
13 Ndipo chizolowezi cha ansembe pakati pa anthu chinali motere
kuti pamene munthu aliyense ankapereka nsembe ndipo nyama ija
ikuwira pa moto, mtumiki wa wansembe ankabwera ndi chifoloko cha
mano atatu m’dzanja lake. 14 Iye ankachipisa mu m’phikamo, ndipo
wansembeyo amatenga chilichonse chimene folokoyo yabaya. Umu ndi
mmene ansembewo amachitira ndi Aisraeli onse amene amabwera ku
Silo. 15 Ndipo ngakhale mafuta asanatenthedwe, mtumiki wansembe
amabwera ndi kunena kwa munthu amene akupereka nsembeyo kuti,
“Ndipatse nyama kuti ndiwotche, pakuti Yehova salandira nyama yophika
koma yayiwisi.”

16 Ngati munthuyo anena kuti, “Apseretu mafuta poyamba, ndipo kenaka mutenge mmene mufunira,” mtumikiyo amayankha kuti, “Ayi ndipatse tsopano lino. Ngati sutero, ine nditenga molanda.”

17 Tchimo la ana a Eli linali lalikulu kwambiri pamaso pa Yehova pakuti iwo amanyoza nsembe za Yehova.

18 Koma Samueli amatumikira pamaso pa Yehova atavala efodi ya
nsalu yofewa yosalala. 19 Chaka chilichonse amayi ake ankamusokera
kamkanjo ndi kukamupatsa akamapita ndi mwamuna wake kukapereka
nsembe za pa chaka. 20 Tsono Eli amadalitsa Elikana ndi mkazi wake
ndi mawu akuti “Yehova akupatseni ana mwa mkazi uyu kulowa m’malo
mwa amene anapempha ndi kumupereka kwa Yehova.” 21 Ndipo Yehova
anamukomera mtima Hana. Anakhala ndi pathupi ndi kubereka ana
aamuna atatu ndi ana aakazi awiri. Ndipo Samueli ankakula pamaso pa
Yehova.

22 Tsono Eli anakalamba kwambiri. Iye ankamva zonse zimene ana
ake aamuna ankachitira Aisraeli onse, ndiponso kuti ankagona ndi akazi
pa chipata cha tenti ya msonkhano. 23 Choncho anawafunsa kuti,
“N’chifukwa chiyani mukuchita zinthu zotere? Ine ndikumva kuchokera
kwa anthu onse za zoyipa zanuzo. 24 Ayi, ana anga si mbiri yabwino
imene ndikumva anthu a Mulungu akufalitsa. 25 Ngati munthu alakwira

munthu mnzake, mwina Mulungu adzamupepesera, koma ngati munthu
achimwira Yehova adzamupepesera ndani?" Koma ana ake sanamvere
kudzudzula kwa abambo awo, pakuti chinali cholinga cha Yehova kuti
awaphe.
26 Ndipo mnyamata Samueli anapitirira kukula mu msinkhu, ndipo
ankapeza kuyanja pamaso pa Yehova ndi anthu.

### *Uneneri Wotsutsa Banja la Eli*

27 Tsiku lina munthu wa Mulungu anabwera kwa Eli ndipo anamuwuza
kuti, "Yehova akuti, 'Kodi Ine sindinadziwulule ndekha kwa banja la
kholo lako pamene iwo anali akapolo a Farao ku Igupto? 28 Ndipo
ndinamusankha pakati pa mafuko a Israeli kuti akhale wansembe wanga
ndi kuti azipita pa guwa langa la nsembe, kufukiza Lubani ndi kuvala efodi
pamaso panga. Ndinapatsa banja la abambo ako gawo la nsembe zonse
zopsereza zimene Aisraeli amapereka. 29 N'chifukwa chiyani ukunyoza
nsembe ndi zopereka zanga zimene ndinalamula? N'chifukwa chiyani
ukupereka ulemu kwa ana ako kuposa Ine podzinenepetsa nokha ndi
zopereka zabwino kwambiri za nsembe zimene Aisraeli amapereka?' "
30 "Paja Ine Yehova Mulungu wa Israeli 'Ndinalonjeza kuti anthu a pa
banja lako ndi a pa banja la abambo ako azidzanditumikira nthawi zonse.'
Koma tsopano ndikuti, 'Zonsezi zithe!' Tsopano anthu amene amandile-
mekeza Inenso ndidzawalemekeza koma iwo amene amandinyoza Ine
ndidzawanyoza. 31 Nthawi ikubwera imene ndidzachotsa anyamata ako
ndi anyamata a pa banja la abambo ako, kotero kuti sipadzakhala
munthu wokalamba pa banja lako. 32 Pa mavuto ako udzayang'ana ndi
maso ansanje zabwino zimene ndidzachitira Aisraeli ena. M'banja lako
simudzapezeka munthu wokalamba. 33 Komabe pa banja lako mmodzi
yekha ndidzamuleka wosamuchotsa kuti azidzanditumikira. Iyeyu azidza-
kuliritsa ndi kukumvetsa chisoni. Koma ena onse pa banja lako adzafa
akanali aang'ono."
34 " 'Ndipo chimene chidzachitike kwa ana ako awiriwa, Hofini ndi
Finehasi, chidzakhala chizindikiro kwa iwe. Onse awiri adzafa pa
tsiku limodzi. 35 Pambuyo pake ndidzasankha wansembe wokhulupirika,
amene adzachita zimene zili mu mtima ndi m'maganizo mwanga.
Ndidzakhazikitsa banja lako kolimba ndipo adzatumikira pamaso pa
wodzozedwa wanga nthawi zonse. 36 Ndipo aliyense wotsala wa banja
lako adzabwera ndi kugwada pamaso pake kupempha ndalama kapena
chakudya.' Adzati, 'Chonde ndiloleni kuti ndizithandizako pa ntchito
iliyonse ya unsembe kuti ndipeze chakudya.' "

## 3

### *Yehova Ayitana Samueli*

1 Samueli ankatumikira Yehova moyang'aniridwa ndi Eli. Masiku
amenewo mawu a Yehova sankamveka pafupipafupi. Kuona zinthu
m'masomphenya sikunkachitikanso kawirikawiri.
2 Tsiku lina Eli, amene maso anali ofowoka ndi kuti sankatha kuona
bwino, anagona pa malo ake. 3 Nthawiyi n'kuti nyale ya Mulungu
isanazimitsidwe. Samueli anali gone mu Nyumba ya Yehova, kumene
kunali Bokosi la Chipangano cha Mulungu. 4 Yehova anayitana Samueli.
Iye anayankha kuti, "Wawa." 5 Ndipo iyeyo anathamangira kwa Eli
ndipo anati, "Ndabwera ndamva kuyitana."

Koma Eli anati, “Ine sindinakuyitane, bwerera kagone.” Ndipo iye
anapita kukagona.

6 Yehova anayitananso, “Samueli!” Ndipo Samueli anadzuka ndi kupita
kwa Eli nati, “Ndabwera popeza ndamva mukundiyitana.”

Eli nati, “Mwana wanga, ine sindinakuyitane, bwerera kagone.”

7 Nthawiyi n’kuti Samueli asanadziwe Yehova ndipo Mawu a Yehova
n’kuti asanawululidwe kwa iye.

8 Yehova anayitananso Samueli kachitatu ndipo Samueli anadzuka
ndikupita kwa Eli ndipo anati, “Ndabwera popeza mwandiyitana ndithu.”

Apo Eli anazindikira kuti Yehova ndiye ankayitana mnyamatayo.
9 Tsono Eli anamuwuza Samueli kuti, “Pita ukagone ndipo akakuyitananso
ukanene kuti, ‘Yankhulani Yehova, pakuti mtumiki wanu ndikumvet-
sera.’ ” Choncho Samueli anapita ndi kukagona pamalo pake.

10 Yehova anabwera ndi kuyima pomwepo, ndi kuyitana monga nthawi
zina zija, “Samueli! Samueli!”

Ndipo Samueli anayankha, “Yankhulani, pakuti mtumiki wanu
akumvetsera.”

11 Ndipo Yehova anati kwa Samueli, “Taona, patsala pang’ono kuti
ndichite chinthu china mu Israeli chimene chidzadabwitsa aliyense amene
adzamve. 12 Tsiku limenelo ndidzachitadi zonse zimene ndinayankhula
zokhudza banja la Eli kuyambira poyamba mpaka pomaliza. 13 Pakuti
ndinamudziwitsa kuti Ine ndikhoza kulanga banja lake kwamuyaya
chifukwa cha zoyipa zimene ana ake ankadziyipitsa nazo. Iye ankadziwa
zimenezi koma osawaletsa. 14 N’chifukwa chake ndinalumbira kuti,
‘Zoyipa zimene banja la Eli linandichita sizidzafafanizidwa mpaka muyaya
ngakhale adzapereke nsembe kapena zopereka zina.’ ”

15 Samueli anagona mpaka mmawa. Atadzuka anatsekula zitseko za
Nyumba ya Yehova. Iye anachita mantha kumuwuza Eli za masomphenya
ake. 16 Koma Eli anamuyitana nati, “Samueli mwana wanga.”

Samueli anayankha kuti, “Wawa.”

17 Tsono Eli anafunsa kuti, “Yehova wakuwuza chiyani? Usandibisire.
Mulungu akulange ndithu ngati undibisira chilichonse cha zimene
wakuwuza.” 18 Choncho Samueli anamuwuza zonse, sanamubisire
kalikonse. Ndipo Eli anati, “Iye ndi Yehova, mulekeni achite chimene
chamukomera.”

19 Yehova anali ndi Samueli pamene amakula, ndipo zonse zimene
ankayankhula zinkachitikadi. 20 Ndipo Aisraeli onse kuyambira ku dera
la Dani mpaka ku Beeriseba anazindikira kuti Yehova analozadi chala pa
Samueli kuti akhale mneneri wake. 21 Yehova anapitiriza kuoneka ku Silo,
ndipo kumeneko anadziwulula yekha kwa Samueli mwa mawu ake.

# 4

1 Ndipo mawu a Samueli anafika kwa Aisraeli onse.

### *Afilisti Alanda Bokosi la Chipangano*

Aisraeli anapita kukamenya nkhondo ndi Afilisti. Aisraeli anamanga
misasa yawo ku Ebenezeri, ndipo Afilisti anamanga ku Afeki. 2 Afilisti
anandanda kuyang’ana Aisraeli nayamba kumenyana. Nkhondo inakula
ndipo Afilisti anagonjetsa Aisraeli napha anthu 4,000 pa malo a nkhon-
dopo. 3 Asilikali atabwerera ku misasa, akuluakulu a Israeli anafunsa
kuti, “N’chifukwa chiyani Yehova walola kuti tigonjetsedwe lero pamaso
pa Afilisti? Tiyeni tikatenge Bokosi la Chipangano cha Yehova ku Silo kuti

Yehovayo abwere kukhala pakati pathu ndi kutipulumutsa m'manja mwa
adani athu."
4 Choncho anatuma anthu ku Silo ndipo anakatenga Bokosi la
Chipangano cha Yehova Wamphamvuzonse amene amakhala pa akerubi.
Ndipo ana awiri a Eli, Hofini ndi Finehasi anatsagana nalo Bokosi la
Chipangano cha Mulungu.
5 Bokosi la Chipangano cha Yehova litafika ku msasa, Aisraeli onse
anafuwula kwambiri mpaka nthaka inagwedezeka. 6 Atamva kufuwulaku,
Afilisti anafunsa, "Kodi kufuwula kwakukulu kumeneku ku misasa ya
Ahebri ndi kwachiyani?"
Atamva kuti Bokosi la Yehova lafika ku msasako, 7 Afilisti anachita man-
tha pakuti iwo ankanena kuti, "Milungu yafika ku msasa. Iwo anati, 'Tili
pamavuto. Chinthu choterechi sichinachitikepo n'kale lomwe. 8 Atsoka
ife! Adzatipulumutsa ndani m'manja mwa milungu yamphamvuyi?
Iyi ndi milungu imene inakantha Aigupto ndi miliri yosiyanasiyana
m'chipululu. 9 Limbani mtima Afilisti! Chitani chamuna, kuti mungakhale
akapolo a Ahebri monga iwowa alili akapolo anu. Chitani chamuna ndipo
menyani nkhondo!' "
10 Choncho Afilisti anamenya nkhondo, ndipo anagonjetsa Aisraeli. Iwo
anathawa aliyense kwawo. Ankhondo a Aisraeli oyenda pansi okwanira
30,000 anaphedwa. 11 Ndipo Bokosi la Chipangano la Yehova linalandidwa,
ndiponso ana awiri Eli, Hofini ndi Finehasi anaphedwa.

### *Imfa ya Eli*

12 Tsiku lomwelo munthu wina wa fuko la Benjamini anathawa ku
nkhondo ndipo anafika ku Silo. Iyeyu zovala zake zinali zong'amba
ndipo anadzithira dothi kumutu kuonetsa chisoni. 13 Atafika, anapeza
Eli atakhala pa mpando wake m'mbali mwa msewu, akungoyang'ana,
pakuti ankadera nkhawa Bokosi la Mulungu. Munthuyo atalowa mu
mzindamo ndi kufotokoza zimene zinachitika ku nkhondo, anthu onse a
mu mzindamo anayamba kulira.
14 Eli atamva kulirako anafunsa kuti, "Kodi phokosoli likutanthauza
chiyani?"
Tsono munthu wa fuko la Benjamini uja anapita msanga kwa Eli
kukamufotokozera. 15 Nthawiyo n'kuti Eli ali wa zaka 98 ndipo maso
ake anali atachita khungu kotero kuti samatha kuona. 16 Munthuyo
anamuwuza Eli kuti, "Ine ndabwera kuchokera ku nkhondo, ndathawako
lero lomwe lino."
Eli anafunsa, "Nanga nkhondo yayenda bwanji mwana wanga?"
17 Iye anayankha kuti, "Aisraeli athawa pamaso pa Afilisti. Anthu
ambirimbiri aphedwa. Ana anunso Hofini ndi Finehasi aphedwa. Bokosi
la Mulungu nalonso lalandidwa."
18 Atangotchula Bokosi la Yehova, Eli anagwa chagada, kuchoka pa
mpando wake umene unali m'mbali mwa chitseko cha mpanda. Khosi lake
linathyoka ndipo anafa, pakuti anali okalamba ndi onenepa kwambiri. Iye
anatsogolera Israeli zaka makumi anayi.
19 Nthawiyo, mpongozi wa Eli, mkazi wa Finehasi anali woyembekezera
ndipo anali pafupi kuchira. Atamva kuti Bokosi la Mulungu lalandidwa
ndi kuti mpongozi wake Eli ndi mwamuna wake amwalira, ululu wa
pobereka mwana unamufikira modzidzimutsa ndipo anabereka mwana.
20 Popeza mkaziyo anali pafupi kumwalira, akazi amene amamuthandiza

anati, “Usaope, wabereka mwana wamwamuna” Koma iye sanayankhe kapena kulabadirako.

21 Tsono iye anatcha mwanayo dzina loti Ikabodi kutanthauza kuti, “Ulemerero wachoka mu Israeli,” chifukwa cha kulandidwa Bokosi la
Mulungu ndi imfa ya mpongozi wake Eli ndi mwamuna wake. 22 Ananena
momwemo kuti, “Ulemerero wachoka mu Israeli, pakuti Bokosi la Mulungu lalandidwa.”

# 5

*Bokosi la Chipangano Pakati pa Afilisti*

1 Afilisti atalanda Bokosi la Mulungu lija, analitenga kuchoka ku
Ebenezeri kupita ku Asidodi. 2 Kenaka anatenga Bokosi la Chipanganolo
nabwera nalo ku nyumba ya Dagoni ndi kuliyika pambali pa Dagoni.
3 Anthu a ku Asidodi atadzuka mmawa mwake, anangoona Dagoni atagwa
pansi chafufumimba pamaso pa Bokosi la Yehova! Iwo anatenga Dagoni
ndi kumuyimika pamalo pake. 4 Koma mmawa mwakenso atadzuka,
anaona Dagoni atagwa chafufumimba pamaso pa Bokosi la Yehova. Mutu
wake ndi manja ake zinali zitaduka ndi kugwera pa khonde polowera,
thunthu lake lokha ndilo linatsala. 5 N’chifukwa chake mpaka lero
ansembe a Dagoni kapena wina aliyense amene amalowa m’kachisi wa Dagoni ku Asidodi saponda pa khonde.

6 Yehova analanga koopsa anthu a ku Asidodi. Yehova anawawononga ndi kuwazunza ndi zithupsa Asidoniwa pamodzi ndi anthu a madera
ozungulira. 7 Anthu a ku Asidodi ataona zimene zimachitika anati, “Bokosi
la Mulungu wa Israeli lisakhale kuno chifukwa akutizunza ife pamodzi ndi
mulungu wathu Dagoni.” 8 Choncho anayitana atsogoleri onse a Afilisti
kuti asonkhane ndipo anawafunsa kuti, “Kodi Bokosi la Mulungu wa Israeli tichite nalo chiyani?”

Iwo anayankha kuti, “Bokosi la Mulungu wa Israeli lipite ku Gati.” Kotero analichotsa Bokosi la Mulungu wa Israelilo.

9 Koma atafika nalo ku Gati, Yehova analanga mzindawo, ndipo anthu
anachita mantha aakulu. Iye anazunza anthu a mu mzindawo, ana ndi
akulu omwe, ndi zithupsa. 10 Choncho anatumiza Bokosi la Mulungu ku Ekroni.

Koma Bokosi la Mulungu lija litangofika ku Ekroni, anthu a ku Ekroni
analira kuti, “Abwera nalo Bokosi la Mulungu wa Israeli kwa ife kuti
atiphe pamodzi ndi anthu athu.” 11 Kotero iwo anayitana atsogoleri onse
a Afilisti kuti asonkhane ndipo anati, “Chotsani Bokosi la Mulungu wa
Israeli, libwerere ku malo ake. Tikapanda kutero lidzatipha ife ndi anthu
athu.” Pakuti mu mzinda monse munali mantha aakulu kwambiri ndipo
Mulungu ankawalanga kwambiri anthu a kumeneko. 12 Anthu amene
sanafe anavutika ndi zithupsa, ndipo kulira kwa anthu a mu mzindamo kunamveka kumwamba.

# 6

*Bokosi la Chipangano Libwerera ku Israeli*

1 Bokosi la Yehova linakhala m’dziko la Afilisti kwa miyezi isanu ndi
iwiri. 2 Tsono Afilisti anayitana ansembe ndi amawula ndipo anati,
“Tichite nalo chiyani Bokosi la Yehova? Tiwuzeni momwe tidzalitumizira ku malo ake.”

3 Iwo anayankha kuti, “Ngati mufuna kubweza Bokosi la Mulungu
wa Israeli, musalitumize wopanda kanthu, koma muyesetse kulitumiza
pamodzi ndi nsembe yopepesera machimo. Mukatero mudzachiritsidwa,
ndipo mudzadziwa chifukwa chiyani chilango cha Yehova sichikuku-
chokani.”

4 Afilisti anafunsanso kuti “Kodi ife tipereke nsembe yanji yopepesera
machimo?”

Iwo anayankha kuti, “Mupereke zifanizo zagolide za zithupsa zisanu
ndi zamakoswe asanu malingana ndi chiwerengero cha akalonga a Afilisti
popeza mliri womwewo wagwera inu ndi akalonga anu. 5 Mupange
zifanizo za zithupsa zisanu ndi za makoswe asanu amene akuwononga
dziko lanu ndipo mupereke ulemu kwa Israeli. Mwina adzaleka kuzunza
inu, milungu yanu ndi dziko lanu. 6 N’chifukwa chiyani mukuwumitsa
mitima monga anachita Aigupto ndi Farao? Mulungu atawalanga anthu a
ku Igupto aja kodi suja anawalola Aisraeli kuti azipita ndipo anapitadi?

7 “Tsopano konzani galeta latsopano limodzi ndiponso ng’ombe ziwiri
zazikazi zamkaka zimene sizinavalepo goli. Muzimangirire ng’ombezo
ku ngoloyo, koma ana awo muwachotse ndi kuwasiya kwanu. 8 Mutenge
Bokosi la Yehova ndi kuliyika pa galetapo ndipo pambali pake pakhale
Bokosi, m’mene muyikemonso zinthu zagolide zomwe mukutumiza kwa
Iye monga nsembe yopepesera machimo. Kenaka, mulisiye lizipita.
9 Koma muziliyang’ana. Ngati lilondola njira yopita kwawo kwa Bokosilo
mpaka ku Beti-Semesi ndiye kuti amene watichita zoyipa zazikulu zoterezi
ndi Mulungu wa Israeli. Koma ngati silitero, ife tidzadziwa kuti
sanali Mulungu wa Israeli amene watizunza koma kuti zinangochitika
mwatsoka.”

10 Anthu aja anachitadi zimenezi. Anatenga ng’ombe zamkaka ziwiri
nazimanga ku galeta lija. Koma ana awo anawatsekera m’khola. 11 Tsono
anayika Bokosi la Yehova pa galeta pamodzi ndi bokosi limene munali
makoswe agolide ndi zifanizo zawo za zithupsa. 12 Ng’ombe zija
zinapita molunjika kutsata msewu wopita ku Beti Semesi zikulira njira
yonse. Sizinakhotere kumanja kapena kumanzere. Akalonga a Afilisti
anazitsatira mpaka m’malire a Beti-Semesi.

13 Nthawi imeneyi anthu a ku Beti-Semesi amakolola tirigu m’chigwa
ndipo pamene anayang’ana ndi kuona Bokosi la Chipangano likubwera
anakondwa. 14 Galeta lija linafika ku munda wa Yoswa ku Beti-Semesi
ndipo linayima. Kumeneko kunali mwala waukulu. Tsono anthu anawaza
nkhuni galetalo, ndipo anapha ng’ombe zija ndi kuzipereka ngati nsembe
zopsereza kwa Yehova. 15 Alevi n’kuti atatsitsa Bokosi la Yehova, pamodzi
ndi bokosi mmene munali zinthu zagolide, ndipo anawayika pa mwala
uja waukulu. Tsiku limenelo anthu a ku Beti-Semesi anapereka nsembe
yopsereza ndi nsembe zina kwa Yehova. 16 Atsogoleri asanu a Afilisti
ataona izi anabwerera ku Ekroni tsiku lomwelo.

17 Zifanizo zagolide za zithupsa zimene Afilisti anatumiza ngati nsembe
zopepesera machimo kwa Yehova zinkayimirira mizinda isanu iyi motere:
chimodzi cha ku Asidodi, china cha ku Gaza ndi zina za ku Asikeloni,
Gati ndi Ekroni. 18 Ndipo chiwerengero cha zifanizo za makoswe chinali
chofanana ndi chiwerengero cha mizinda ya akalonga asanu a Afilisti.
Mizindayi inali yotetezedwa bwino ndi ina yapamtetete. Mwala waukulu
umene anayikapo Bokosi la Chipangano la Yehova m’munda mwa Yoswa
ku Beti-Semesi uli ngati mboni mpaka lero.

19 Yehova anakantha amuna a ku Beti-Semesi 70 chifukwa anasuzumira
m'Bokosi la Chipangano cha Yehova. Ndipo anzawo analira chifukwa
Yehova anawalanga kwambiri. 20 Tsono anthu a ku Beti-Semesi anafunsa,
"Ndani angathe kuyima pamaso pa Yehova Mulungu Woyera? Bokosi la
Chipanganoli lipita kuti likachoka pano?"
21 Tsono iwo anatumiza a mithenga kwa anthu a ku Kiriati-Yearimu kuti,
"Afilisti atibwezera Bokosi la Yehova. Bwerani kuno mudzalitenge, mupite
nalo kwanuko."

# 7

1 Choncho anthu a ku Kiriati-Yearimu anabwera ndi kudzatenga Bokosi
la Yehova. Iwo anapita nalo ku nyumba ya Abinadabu ya ku phiri ndipo
anapatula Eliezara mwana wake kuti aziyang'anira Bokosi la Yehovalo.

### *Samueli Agonjetsa Afilisti ku Mizipa*

2 Zaka makumi awiri zinapita kuyambira pamene Bokosi la Yehova
linakhala ku Kiriati-Yearimu, ndipo anthu a Israeli onse analira kupempha
Yehova kuti awathandize. 3 Ndipo Samueli anati kwa nyumba yonse
ya Israeli, "Ngati mukubwerera kwa Yehova ndi mtima wanu wonse,
muchotse milungu yachilendo ndi Asiteroti pakati panu ndipo mitima
yanu ikhazikike pa Yehova ndi kutumikira Iye yekha. Mukatero Iye
adzakupulumutsani m'manja mwa Afilisti." 4 Choncho Aisraeli anachotsa
milungu yawo ya Baala ndi Asitoreti ndi kutumikira Yehova yekha.
5 Kenaka Samueli anati, "Sonkhanitsani Aisraeli onse ku Mizipa ndipo
ine ndidzakupemphererani kwa Yehova." 6 Choncho anasonkhana ku
Mizipa, ndipo anatunga madzi ndi kuwathira pansi pamaso pa Yehova.
Pa tsiku limenelo anasala kudya namanena kuti, "Ife tachimwira Yehova."
Ndipo Samueli anali mtsogoleri wa Israeli ku Mizipa.
7 Afilisti anamva kuti Aisraeli asonkhana ku Mizipa, choncho akalonga
awo anabwera kudzawathira nkhondo. Ndipo Aisraeli atamva anachita
mantha chifukwa cha Afilisti. 8 Choncho anati kwa Samueli, "Musasiye
kutipempherera kwa Yehova Mulungu wathu, kuti atipulumutse m'dzanja
la Afilistiwa." 9 Ndipo Samueli anatenga mwana wankhosa wamkazi
woyamwa ndi kumupereka monga nsembe yopsereza kwa Yehova. Iye
anapemphera kwa Yehova m'malo mwa Aisraeli, ndipo Yehova ana-
muyankha.
10 Samueli akupereka nsembe yopsereza, Afilisti anayandikira kuti
ayambe kuwathira nkhondo Aisraeli. Koma tsiku limenelo Yehova
anawaopseza Afilisti aja ndi mawu aakulu ngati bingu. Choncho
anasokonezeka motero kuti Aisraeli anawagonjetsa. 11 Aisraeli anatuluka
ku Mizipa kuthamangitsa Afilisti aja n'kumawapha m'njira yonse mpaka
kumunsi kwa Beti-Kari.
12 Kenaka Samueli anatenga mwala nawuyika pakati pa Mizipa ndi Seni.
Iye anawutcha Ebenezeri, popeza anati, "Yehova watithandiza mpaka
pano." 13 Kotero Afilisti anagonjetsedwa ndipo sanadzalowenso m'dziko
la Israeli.
Yehova analimbana ndi Afilisti masiku onse a Samueli. 14 Mizinda
yonse imene Afilisti analanda kuchokera ku Ekroni mpaka ku Gati
inabwezedwa kwa Aisraeli. Choncho Aisraeli anapulumutsa dziko lawo.
Ndipo panalinso mtendere pakati pa Aisraeli ndi Aamori.
15 Samueli anatsogolera Aisraeli moyo wake wonse. 16 Chaka ndi chaka
Samueli ankakonza ulendo wozungulira kuchokera ku Beteli mpaka ku
Giligala ndi Mizipa, kuweruza milandu ya Aisraeli m'madera onsewa.

17 Koma pambuyo pake ankabwerera ku Rama, kumene kunali nyumba
yake. Ankaweruza Aisraeli kumeneko. Ndipo iye anamanga guwa
lansembe la Yehova kumeneko.

# 8

## *Aisraeli Apempha kuti Akhale ndi Mfumu*

1 Samueli atakalamba anasankha ana ake kuti akhale oweruza Ais-
raeli. 2 Mwana wake woyamba anali Yoweli, wachiwiri anali Abiya,
ndipo ankaweruza ku Beeriseba. 3 Koma ana akewo sanatengere
makhalidwe ake abwino. Iwo ankapotokera ku zoyipa namatsata phindu
mwachinyengo. Ankalandira ziphuphu ndi kumaweruza mwachinyengo.

4 Tsono akuluakulu onse a Israeli anasonkhana pamodzi ndipo an-
abwera kwa Samueli ku Rama. 5 Iwo anati kwa iye "Taonani, inu
mwakula tsopano ndipo ana anu sakutsata makhalidwe anu abwino.
Tsono mutipatse mfumu kuti izitilamulira, monga momwe ikuchitira
mitundu ina yonseyi."

6 Koma mawu oti, "Mutipatse mfumu kuti izitilamulira," sanakondw-
eretse Samueli. Choncho anapemphera kwa Yehova. 7 Yehova ana-
muyankha nati, "Mvera zonse zimene anthuwa akukuwuza. Si ndiwe
amene akumukana, koma akukana Ine kuti ndikhale mfumu yawo.
8 Kuyambira tsiku limene ndinawatulutsa m'dziko la Igupto mpaka
lero zochita zawo zakhala zondikana Ine n'kumatumikira milungu ina.
Tsopano akukukananso iwe. 9 Tsono amvere zimene akunena, koma
uwachenjeze kwambiri ndipo uwawuzitse za khalidwe la mfumu imene
idzawalamulire."

10 Samueli anawawuza anthu amene amamupempha mfumu aja mawu
onse a Yehova. 11 Iye anati, "Zimene mfumu imene idzakulamulireniyo
idzachite ndi izi: Izidzatenga ana anu aamuna kuti akhale ankhondo ake;
ena pa magaleta ake, ena pa akavalo ake ndipo ena othamanga patsogolo
pa magaleta akewo. 12 Ena adzawayika kukhala olamulira asilikali 1,000,
ena olamulira asilikali makumi asanu, ndi ena otipula minda yake, ndi
kukolola ndiponso ena adzakhala osula zida zankhondo ndi zida za
magaleta ake. 13 Iyo idzatenga ana anu akazi kuti akhale oyenga mafuta
onunkhira, ophika chakudya ndi kupanga buledi. 14 Idzatenga minda
yanu yabwino ya mpesa ndi ya mitengo ya olivi ndipo adzayipereka kwa
antchito ake. 15 Idzatenga gawo lakhumi la tirigu wanu ndi mphesa zanu
ndi kupereka kwa nduna zake ndi akapitawo ake. 16 Mfumuyo idzatenga
antchito anu aamuna ndi aakazi. Idzatenganso ng'ombe zanu zabwino
ndi abulu anu n'kumazingwiritsa ntchito. 17 Iyo idzatenga gawo lakhumi
la zoweta zanu, ndipo inu eni mudzakhala akapolo ake. 18 Nthawi imeneyo
ikadzafika inu mudzalira momvetsa chisoni chifukwa cha mfumu imene
mwadzisankhira, koma Yehova sadzakuyankhani."

19 Koma anthu anakana kumumvera Samueli. Iwo anati, "Ayi! Ife
tikufuna mfumu yotilamulira. 20 Kotero ifenso tidzakhala ngati mayiko
ena. Mfumu yathu idzatiweruza ndiponso idzatuluka nafe kutitsogolera
kukamenya nkhondo."

21 Samueli atamva zonse zimene anthuwo ananena, iye anakazifo-
tokozanso kwa Yehova. 22 Yehova anamuyankha nati, "Amvere zimene
akunena ndipo apatse mfumu."

Ndipo Samueli anati kwa Aisraeli aja, "Bwererani aliyense kwawo."

# 9

*Samueli Adzoza Sauli*

1 Panali munthu wina wa fuko la Benjamini, wotchuka, dzina lake
Kisi, mwana wa Abieli, mwana wa Zerori, mwana wa Bekorati, mwana
wa Afiya. 2 Iyeyu anali ndi mwana dzina lake Sauli, mnyamata wa
maonekedwe abwino. Pakati pa Aisraeli onse panalibe wofanana naye.
Anali wamtali kotero kuti anthu onse ankamulekeza m'mapewa.

3 Tsono abulu a Kisi, abambo ake a Sauli anasowa. Choncho Kisi
anati kwa mwana wake Sauli, "Tenga wantchito mmodzi ndipo mupite
mukafunefune abuluwo." 4 Choncho iwo anadutsa dziko la mapiri a
Efereimu ndi dera la Salisa, koma sanawapeze. Anadutsa ku Saalimu
koma abuluwo sanawapeze. Kenaka anadutsa dziko la Benjamini, koma
osawapezabe.

5 Atafika ku dera la Zufi, Sauli anawuza mnyamata wake kuti, "Tiye
tibwerere, mwina abambo anga angasiye kudandaula za abulu ndipo
adzayamba kudandaula za ife."

6 Koma mnyamatayo anayankha kuti, "Taonani, mu mzinda uwo muli
munthu wa Mulungu. Anthu amamupatsa ulemu kwambiri, ndipo zonse
zimene amanena zimachitika. Tiyeni tipite kumeneko tsopano. Mwina
adzatiwuza kumene tiyenera kulowera."

7 Sauli anafunsa mnyamata wake kuti, "Tikapita tikamupatsa chiyani
munthuyo pakuti chakudya chimene chinali m'matumba mwathu chatha?
Tilibe mphatso iliyonse yoti timutengere munthu wa Mulungu. Nanga tili
ndi chiyani?"

8 Mnyamatayo anayankha kuti, "Onani, ndili ndi kandalama kakang'ono
ka siliva. Ndikamupatsa munthu wa Mulunguyo ndipo akatidziwitsa
kumene kuli abuluwo." 9 (Kale mu Israeli ngati munthu afuna kukapem-
pha nzeru kwa Mulungu ankanena kuti, "Tiyeni tipite kwa mlosi." Ndiye
kuti munthu amene lero akutchedwa mneneri, kale ankatchedwa mlosi).
10 Tsono Sauli anawuza mnyamata wake kuti, "Chabwino, tiye tipite."
Ndipo ananyamuka kupita ku mzinda umene kunali munthu wa Mulun-
guyo.

11 Akukwera phiri kupita ku mzindawo anakumana ndi atsikana
akutuluka mu mzindamo kukatunga madzi, ndipo anawafunsa kuti, "Kodi
mlosi uja alipo?"

12 Iwo anayankha, "Inde alipo. Ali kutsogolo kwanuku, fulumirani
tsopano, wangobwera kumene mu mzinda wathu uno lero, chifukwa
lero anthu akupereka nsembe ku phiri. 13 Mukangolowa mu mzindawo
mumupeza asanapite ku phiri kukadya. Anthu sangayambe kudya
iye asanabwere chifukwa iyeyu ayenera kudalitsa nsembeyo. Kenaka
anthu oyitanidwa adzayamba kudya. Pitani tsopano, chifukwa muyenera
kumupeza nthawi ino."

14 Choncho anapita ku mzinda kuja. Akulowa mu mzindamo, anaona
Samueli akutuluka mu mzindamo akubwera kumene kunali iwo, koma
amapita ku phiri, ku malo wopatulika.

15 Koma chadzulo lake Sauli asanafike, Yehova anali atamuwuza kale
Samueli za zimenezi kuti, 16 "Mawa nthawi ngati yomwe ino ndidza-
kutumizira munthu wochokera ku dziko la Benjamini. Udzamudzoze
kuti akhale mtsogoleri wa anthu anga, Aisraeli. Iye adzawapulumutsa
m'dzanja la Afilisti. Ine ndaona kuzunzika kwawo ndipo ndamva kulira
kwawo."

17 Samueli atamuona Sauli, Yehova anamuwuza kuti, “Munthu ndi-
nakuwuza uja ndi uyu. Iyeyu adzalamulira anthu anga.”
18 Tsono Sauli anayandikira Samueli pa chipata ndipo anamufunsa,
“Kodi mungandiwuze kumene kuli nyumba ya mlosi?”
19 Samueli anayankha, “Ine ndine mlosiyo. Tsogolani kupita ku phiri
pakuti lero mudya ndi ine, ndipo mawa mmawa ndidzakuwuzani zonse
zimene zili mu mtima mwanu. 20 Musadere nkhawa za abulu anu amene
akhala akusowa masiku atatu apitawa, poti apezeka kale. Kodi Aisraeli
onse akufunitsitsa ndani? Kodi si ndiwe ndi nyumba yonse ya abambo
ako?”
21 Sauli anayankha, “Inetu ndine Mbenjamini, fuko laling’ono la mafuko
onse a Israeli, ndipo banja langa ndi laling’ono pakati pa mabanja a fuko
la Benjamini. Nanga n’chifukwa chiyani mukunena zimenezi kwa ine?”
22 Ndipo Samueli anatenga Sauli ndi mnyamata wake uja ndi kulowa
nawo m’chipinda chachikulu ndipo anawakhazika kutsogolo kwa anthu
oyitanidwa. Onse pamodzi analipo anthu makumi atatu. 23 Tsono Samueli
anati kwa wophika, “Bwera nayo nyama imene ndinakupatsa, imene
ndinakuwuza kuti uyisunge pambali.”
24 Kotero wophikayo anatenga mwendo wa nyama ndipo anawuyika
patsogolo pa Sauli. Samueli anati “Nayi nyama imene ndinakusungira
kuti pa nthawi yake udye pamodzi ndi anthu amene ndawayitana.” Ndipo
Sauli anadya tsiku limenelo ndi Samueli.
25 Atatsika kuchoka ku phiri kuja, Samueli anamukonzera Sauli malo
ogona pa denga la nyumba yake, ndipo Sauli anagona pamenepo. 26 Tsono
m’bandakucha Samueli anayitana Sauli pa dengapo nati, “Konzeka ndipo
ine ndikuperekeza.” Choncho Sauli anadzuka ndipo onse awiri, Samueli
ndi Sauli anakalowa mu msewu. 27 Atakafika ku mathero a mzindawo,
Samueli anati kwa Sauli, “Muwuzeni mnyamata wanu kuti atsogole,
koma inuyo muyime pang’ono kuti ndikuwuzeni mawu ochokera kwa
Mulungu.”

# 10

1 Ndipo Samueli anatenga botolo la mafuta nathira mafutawo pa mutu
wa Sauli ndipo anapsompsona nati, “Yehova wakudzoza kuti ukhale
mtsogoleri wa anthu ake, Aisraeli. Iwe udzalamulira anthu a Yehova
ndiponso udzawapulumutsa m’manja mwa adani awo owazungulira.
Chizindikiro chakuti Yehova wakudzoza kuti ukhale mtsogoleri wa anthu
ake ndi ichi: 2 Ukachoka pano lero lino, udzakumana ndi amuna awiri
kufupi ndi manda a Rakele ku Zeliza m’malire mwa dziko la Benjamini
ndipo adzakuwuza kuti, ‘Abulu amene munkafunafuna aja apezeka.
Ndipo tsopano abambo ako asiya kuganiza za abulu ndipo akudera
nkhawa za iwe.’ Iwo akufunsa kuti, ‘Kodi ndidzachita chiyani mmene
mwana wanga sakuoneka?’ ”
3 “Ndipo udzapyola pamenepo ndi kufika ku mtengo wa thundu wa
ku Tabori. Kumeneko udzakumana ndi anthu atatu akupita kukapereka
nsembe ku Nyumba ya Mulungu ku Beteli. Mmodzi adzakhala atanyamula
ana ambuzi atatu, wina atanyamula malofu atatu a buledi, ndi winayo
atanyamula thumba la vinyo. 4 Adzakupatsa moni ndi kukupatsa malofu
awiri a buledi. Iwe udzalandire bulediyo.
5 “Pambuyo pake, udzafike ku Gibeyati-Elohimu, kumene kuli gulu la
ankhondo la Afilisti. Pamene ukuyandikira mzindawo, udzakumana ndi
gulu la aneneri akutsika kuchokera ku phiri, akuyimba zeze, ng’oma,

zitoliro ndi pangwe, ndiponso akulosera. 6 Kenaka Mzimu wa Yehova
udzabwera pa iwe ndi mphamvu, ndipo udzayamba kulosera nawo
pamodzi. Ndipo udzasinthika kukhala munthu wina. 7 Zizindikiro izi
zikakachitika, dzachite chilichonse manja ako angathe kuchita, pakuti
Mulungu ali nawe.
8 "Tsono tsogola kupita ku Giligala. Ine ndidzabwera ndithu kudza-
pereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano. Koma ukandidikire
masiku asanu ndi awiri mpaka ine nditabwera kuti ndidzakuwuze zomwe
udzachite."

### *Sauli Avekedwa Ufumu*

9 Sauli akutembenuka kusiyana ndi Samueli, Mulungu anasintha
mtima wa Sauli, ndipo zinthu zonsezi zinakwaniritsidwa tsiku lomwelo.
10 Atafika ku Gibeya, anakumana ndi gulu la aneneri. Mzimu wa Mulungu
unabwera pa iye mwamphamvu, nayamba kulosa nawo. 11 Pamene onse
amene ankamudziwa kale anamuona akulosera pamodzi ndi aneneri,
anafunsana wina ndi mnzake. "Kodi n'chiyani chachitika ndi mwana wa
Kisi? Kodi Sauli alinso m'gulu la aneneri?"
12 Munthu wina wa kumeneko anayankha kuti, "Nanga enawa abambo
awo ndani?" Kotero kunayambika mwambi wakuti, "Kodi Saulinso ali
m'gulu la aneneri?" 13 Sauli atasiya kuloserako, anapita ku kachisi ku
phiri.
14 Tsono amalume ake a Sauli anamufunsa ndi mnyamata wake kuti,
"Munapita kuti?"
Iye anayakha, "Timakafunafuna abulu koma titaona kuti sakupezeka,
tinapita kwa Samueli."
15 Amalume ake a Sauli anati, "Chonde, ndifotokozereniko zimene
Samueli wakuwuzani."
16 Sauli anati, "Iye anatitsimikizira kuti abulu anapezeka." Koma
sanawawuze amalume akewo za nkhani ija ya ufumu imene Samueli
anamuwuza.
17 Samueli anayitana Aisraeli onse kuti asonkhane pamaso pa Yehova ku
Mizipa. 18 Ndipo anawuza Aisraeli onse kuti, "Yehova Mulungu wa Israeli
akuti, 'Ine ndinakutulutsani m'dziko la Igupto ndi kukupulumutsani
m'dzanja la Igupto ndi m'dzanja la mafumu onse amene ankakuzunzani.'
19 Koma lero mwamukana Mulungu wanu amene amakupulumutsani
m'mavuto anu onse ndi m'zowawa zanu. Ndipo mukuti, 'Ayi, koma
mutipatse mfumu yotilamulira.' Tsopanotu sonkhanani pamaso pa
Yehova mwa mafuko ndi mabanja anu."
20 Samueli atasonkhanitsa mafuko onse a Israeli, fuko la Benjamini
linasankhidwa. 21 Anasonkhanitsa fuko la Benjamini banja ndi banja.
Pomaliza anasonkhanitsa banja la Matiri mmodzimmodzi ndipo Sauli
mwana wa Kisi anasankhidwa. Koma atamufunafuna, sanamupeze.
22 Tsono anthu anafunsanso kwa Yehova kuti, "Kodi munthuyu wabwera
kale kuno?"
Ndipo Yehova anayankha kuti, "Inde wabisala pakati pa katundu."
23 Iwo anathamanga ndi kukamutenga kumeneko. Atayimirira pakati
pa anthu anapezeka kuti anali wamtali kuposa anthu ena mwakuti
ankamulekeza m'mapewa. 24 Samueli anafunsa anthu onse kuti, "Kodi
mukumuona munthu amene Yehova wasankha? Palibe wofanana naye
pakati pa anthu onse."
Kenaka anthu onse anafuwula kuti, "Mfumu ikhale ndi moyo wautali!"

25 Samueli anafotokozera anthu ntchito ndi udindo wa mfumu. Pam-
buyo pake analemba m'buku zonse zokhudza ntchito ndi udindo wa
mfumu, ndipo bukulo analiyika pamaso pa Yehova. Kenaka Samueli
analola aliyense kuti abwerere kupita kwawo.
26 Sauli anapitanso ku mudzi kwawo ku Gibeya, pamodzi ndi anthu
amphamvu amene Mulungu anawafewetsa mitima. 27 Koma anthu
ena achabechabe anati, "Kodi munthu uyu angathe bwanji kutipu-
lumutsa?" Iwo anayamba kumunyoza Sauliyo, ndipo sankamupatsa
ngakhale mphatso. Koma iye sanalabadireko.

# 11

### *Sauli Apulumutsa Mzinda wa Yabesi*

1 Nahasi, Mwamoni anapita ndi kuzungulira mzinda wa Yabesi Giliyadi.
Tsono anthu onse a ku Yabesi anapempha Nahasiyo kuti, "Muchite nafe
pangano, ndipo tidzakutumikirani."
2 Koma Nahasi Mwamoni uja anayankha kuti, "Ndidzachita nanu
pangano pokhapokha nditakolowola diso lakumanja la aliyense wa inu
kuti ndichititse manyazi Aisraeli onse."
3 Akuluakulu a mzinda wa Yabesi anati kwa iye, "Utipatse masiku asanu
ndi awiri kuti titumize uthenga mu Israeli monse. Ngati sipapezeka
wodzatipulumutsa, ndiye ife tidzadzipereka kwa iwe."
4 Amithenga aja atafika kwawo kwa Sauli ku Gibeya ndi kufotokoza
nkhaniyi kwa anthu onse, iwo analira motaya mtima. 5 Pa nthawiyo
n'kuti Sauli akubwera kuchokera ku munda, ali pambuyo pa ng'ombe zake
za ntchito ndipo anafunsa. "N'chiyani chawavuta anthuwa kuti azilira
motere?" Ndipo anamufotokozera zomwe anthu a mu mzinda wa Yabesi
ananena.
6 Sauli atamva mawu awo, Mzimu wa Mulungu unabwera pa iye mwa
mphamvu ndipo anakwiya kwambiri. 7 Tsono anatenga ng'ombe ziwiri za
ntchito, nazidula nthulinthuli. Ndipo anatumiza amithenga ndi nthulizo
dziko lonse la Israeli ndi mawu akuti, "Umo ndi mmene adzachite ndi
ng'ombe ya aliyense amene satsata Sauli ndi Samueli." Ndipo anthu
anachita mantha aakulu motero kuti onse ananyamuka ndi mtima umodzi.
8 Pamenepo Sauli anawasonkhanitsa ku Bezeki nawawerenga, ndipo
Aisraeli analipo 300,000, Ayuda analipo 30,000.
9 Tsono Sauli anawuza amithenga ochokera ku Yabesi aja kuti,
"Mukawawuze anthu a ku Yabesi Giliyadi kuti mawa nthawi ya masana
adzapulumutsidwa." Pamene amithengawo anapita ndi kukafotokoza
nkhani imeneyi kwa anthu a ku Yabesi, iwo anasangalala kwambiri.
10 Choncho anthu a ku Yabesi anawuza Nahasi kuti, "Mawa tidzadzipereka
kwa inu ndipo inu mudzachite nafe chilichonse chokukomerani."
11 Tsono mmawa mwake Sauli anagawa anthuwo m'magulu atatu.
Mmamawa kusanache iwo analowa m'misasa ya Aamoni ndi kuwapha
mpaka masana. Amene anapulumuka anabalalika, aliyense kwakekwake.

### *Sauli Avomerezedwa kukhala mfumu*

12 Kenaka anthu anafunsa Samueli kuti, "Kodi ndani aja ankanena kuti,
'Kodi Sauli n'kutilamulira ife?' Bwera nawoni kuno kuti tidzawaphe."
13 Koma Sauli anati, "Palibe amene ati aphedwe lero, pakuti lero lino
Yehova wagwira ntchito yopulumutsa Israeli."

14 Ndipo Samueli anati kwa anthuwo, “Tiyeni tipite ku Giligala kuti
tikatsimikizenso kuti Sauli ndi mfumu yathu.” 15 Choncho anthu onse
anapita ku Giligala ndipo kumeneko Samueli anakalonga Sauli ufumu
pamaso pa Yehova. Pambuyo pake anthu anapereka nsembe zachiyanjano
pamaso pa Yehova, ndipo Sauli ndi Aisraeli onse anachita chikondwerero
chachikulu.

# 12

*Samueli Atsanzika Anthu*

1 Pambuyo pake Samueli anawuza Aisraeli onse kuti, “Ine ndamvera
zonse zimene munandiwuza ndipo ndakupatsani mfumu kuti izikula-
mulirani. 2 Tsopano muli ndi mfumu imene izikutsogolerani, koma ine
ndakalamba, kumutu kwanga kuli imvi zokhazokha ndipo ana anga
ali pamodzi ndi inu. Ndakhala ndili mtsogoleri wanu kuyambira ndili
mnyamata mpaka lero. 3 Ine ndili pano. Ngati ndinalakwa chilichonse
nditsutseni pamaso pa Yehova ndi wodzozedwa wake. Kodi ndinalanda
ng’ombe ya yani? Kodi ndinalanda bulu wa yani? Kodi ndani amene
ndinamudyera masuku pa mutu? Kodi ndinazunza yani? Kodi ndina-
landira kwa yani chiphuphu choti n’kundidetsa m’maso? Ngati ndinachita
chilichonse cha izi, ine ndidzakubwezerani.”

4 Iwo anayankha kuti, “Inu simunatidyere masuku pamutu kapena
kutizunza. Simunalande kanthu kalikonse ka munthu.”

5 Samueli anawawuza kuti, “Yehova ndiye mboni pakati pa inu ndi ine,
ndiponso wodzozedwa wake ndi mboni kuti lero simunapeze chilichonse
m’dzanja langa.”

Iwo anati, “Inde, Yehova ndiye mboni.”

6 Samueli anawawuzanso kuti, “Yehova ndiye amene anasankha Mose
ndi Aaroni kuti atulutse makolo anu m’dziko la Igupto. 7 N’chifukwa chake
tsopano imani pomwepa kuti ndikufotokozereni pamaso pa Yehova, za
ntchito za chipulumutso zimene Yehova anachitira inu ndi makolo anu.

8 “Yakobo atapita ku dziko la Igupto, Aiguptowo akuwazunza, iwo
analirira kwa Yehova kuti awathandize, ndipo Yehova anatumiza Mose
ndi Aaroni, amene anatulutsa makolo anu m’dziko la Igupto ndi kudza-
wakhazika pa malo ano.

9 “Koma iwo anayiwala Yehova Mulungu wawo, choncho Yehova
anawapereka m’dzanja la Sisera mkulu wa ankhondo wa mzinda wa
Hazori, ndiponso m’manja mwa Afilisti ndi mfumu ya Mowabu. Mafumu
onsewa anathira nkhondo makolo anu. 10 Tsono iwo analira kwa Yehova
nati, ‘Ife tachimwa, chifukwa tamusiya Yehova ndi kumatumikira mafano
a Baala ndi Asiteroti. Koma tsopano tilanditseni m’manja mwa adani
athu ndipo tidzakutumikirani.’ 11 Choncho Yehova anatumiza Yeru-Baala,
Bedani, Yefita ndi Samueli ndipo anakulanditsani m’manja mwa adani anu
amene anakuzungulirani, kotero munakhala mwamtendere.

12 “Koma mutaona kuti Nahasi mfumu ya Amoni inkabwera kudza-
menyana nanu, inu munandiwuza kuti, ‘Ayi, ife tikufuna mfumu kuti
itilamulire,’ ngakhale kuti Yehova Mulungu wanu ndiye anali mfumu
yanu. 13 Tsopano nayi mfumu imene mwayisankha, imene munayipem-
pha. Onani, Yehova wakupatsani mfumu. 14 Ngati muziopa Yehova ndi
kumamutumikira ndi kumamumvera, osamupandukira ndiponso ngati
inu pamodzi ndi mfumu yanu mudzatsata Yehova Mulungu wanu, ndiye
zinthu zonse zidzakuyenderani bwino. 15 Koma mukapanda kumvera

Yehova ndi kumupandukira, ndiye adzakulangani pamodzi ndi mfumu
yanu yomwe.
16 “Tsono imani pomwepa kuti muone chinthu chachikulu chimene
Yehova ali pafupi kuchita pamaso panu! 17 Kodi ino si nthawi yokolola
tirigu? Komabe ndipemphera kwa Yehova kuti agwetse mvula ya
mabingu. Zikatero mudzadziwa kuti tchimo lanu limene mwachita
popempha mfumu kwa Yehova ndi lalikulu.”
18 Choncho Samueli anapemphera, ndipo Yehova anatumiza mvula ya
mabingu tsiku lomwelo. Apo anthu aja anaopa kwambiri Yehova ndi
Samueli.
19 Tsono anamupempha Samueli nati, “Chonde mutipempherere kwa
Yehova, ife atumiki kuti tingafe pakuti pa machimo athu onse tawonjezapo
tchimo lopempha mfumu.”
20 Samueli anayankha kuti, “Musaope, inu mwachitadi tchimo ili,
koma musaleke kumutsata Yehova ndi kumutumikira ndi mtima wanu
wonse. 21 Ndipo musatsate mafano achabechabe amene alibe phindu
ndipo sangakupulumutseni popeza ndi achabechabe. 22 Yehova adzakana
anthu ake kuopa kuti dzina lake lamphamvu linganyozeke, pakuti
chinamukondweretsa Yehova kuti akusandutseni inu kukhala anthu ake.
23 Ndiponso kunena za ine, zisachitike kuti ndichimwire Yehova pakule-
phera kukupemphererani. Ndipo ine ndidzakuphunzitsani njira yabwino
ndi yolungama kuti muziyendamo. 24 Koma onetsetsani kuti mukuopa
Yehova ndi kumutumikira mokhulupirika ndi mtima wanu wonse. Nthawi
zonse muziganizira zinthu zazikulu wakhala akukuchitirani. 25 Komabe
mukapitirira kuchita zoyipa, ndiye kuti inu pamodzi ndi mfumu yanu
mudzachotsedwa.”

# 13

*Samueli Adzudzula Sauli*

1 Sauli analowa ufumu ali ndi zaka makumi atatu, ndipo analamulira
Israeli kwa zaka 42.
2 Nthawi ina Sauli anasankha Aisraeli 3,000. Mwa iwowa, 2,000 anali
ndi Sauliyo ku Mikimasi ndi ku dziko la mapiri ku Beteli, ndipo 1,000 anali
ndi Yonatani ku Gibeya ku Benjamini. Anthu ena onse otsala anawabweza
kwawo.
3 Yonatani anakantha mkulu wa ankhondo wa Afilisti ku Geba, ndipo
Afilisti anamva kuti Aheberi awukira. Tsono Sauli anawuza amithenga
kuti alize lipenga m’dziko lonse la Israeli. 4 Choncho Aisraeli onse anamva
kuti Sauli wakantha mkulu wa ankhondo Wachifilisiti ndi kuti Afilisti
anayipidwa nawo Aisraeli. Ndiye anthu anayitanidwa kuti abwere kwa
Sauli ku Giligala.
5 Tsono Afilisti anasonkhana kuti amenyane ndi Aisraeli. Iwo anali ndi
magaleta 3,000, okwera pa akavalo 2,000 ndiponso asilikali kuchuluka
kwake ngati mchenga wa m’mbali mwa nyanja. Iwo anapita ndi kuka-
manga misasa yawo ku Mikimasi, kummawa kwa Beti-Aveni. 6 Pamene
Aisraeli anaona kuti anali pamavuto akulu, poti anali atapanikizidwa
kwambiri, anabisala m’mapanga, m’maenje, m’matanthwe, m’makwalala
ndi m’zitsime. 7 Ahebri ena anawoloka Yorodani mpaka kukafika ku dziko
la Gadi ndi ku Giliyadi.
Koma Sauli anakhalabe ku Giligala ndipo ankhondo onse amene anali
naye anali njenjenje ndi mantha. 8 Saulo anadikirira masiku asanu
ndi awiri, monga mwa nthawi imene ananena Samueli. Koma Samueli

sanabwere ku Giligala, ndipo anthu anayamba kumuthawa Sauli uja.
9 Kotero iye anati, “Bwera nayoni nsembe yopsereza ndi nsembe ya
chiyanjano.” Ndipo Sauli anapereka nsembe yopsereza. 10 Atangomaliza
kupereka nsembe, anangoona Samueli watulukira ndipo Sauli anapita
kukamulonjera.

11 Samueli anafunsa kuti, “N’chiyani chimene wachita?”

Sauli anayankha kuti, “Nditaona kuti anthu ayamba kundithawa, ndi
kuti inu simunabwere pa nthawi munanena ija, ndiponso kuti Afilisti
akusonkhana ku Mikimasi, 12 ndinati, ‘Tsopano Afilisti abwera kudzan-
dithira nkhondo ku Giligala kuno, chonsecho sindinapemphe Yehova
kuti andikomere mtima.’ Motero ndinakakamizika kupereka nsembe
yopsereza.”

13 Samueli anati, “Mwachita zopusa. Simunatsate zimene Yehova
Mulungu wanu anakulamulani kuti muchite. Mukanazitsata, Yehova
akanawukhazikitsa ufumu wanu mu Israeli mpaka kalekale. 14 Koma
tsopano ufumu wanu sudzakhalitsa. Yehova wapeza munthu wapamtima
pake ndipo wamusankha kukhala mtsogoleri wa anthu ake chifukwa inu
simunasunge malamulo a Yehova.”

15 Kenaka Samueli anachoka ku Giligala ndi kupita ku Gibeyati ku dziko
la Benjamini. Saulo anawerenga anthu amene anali naye ndipo analipo
600.

*Sauli Akonzekera Nkhondo*

16 Sauli ndi mwana wake Yonatani pamodzi ndi asilikali amene anali
naye aja amakhala ku Geba ku dziko la Benjamini. Koma Afilisti anamanga
misasa yawo ku Mikimasi. 17 Ankhondo a Afilisti anatuluka m’misasa
yawo m’magulu atatu. Gulu lina linapita ku Ofiri ku dziko la Suwala.
18 Gulu lina linalunjika ku Beti-Horoni, ndipo gulu lachitatu linalunjika ku
malire oyang’anana ndi chigwa cha Zeboimu cha ku chipululu.

19 Nthawi imeneyo n’kuti mulibe osula zitsulo m’dziko lonse la Israeli,
pakuti Afilisti anati, “Tisawalole Aheberi kudzipangira okha malupanga
kapena mikondo!” 20 Kotero Aisraeli onse amapita kwa Afilisti kukanoletsa
mapulawo, makasu, nkhwangwa ndi zikwakwa zawo. 21 Mtengo wonolera
mapulawo ndi makasu unali zigawo ziwiri za sekeli, mtengo wonolera
zisonga ndi nkhwangwa unali gawo limodzi la Sekeli.

22 Motero tsiku la nkhondolo panalibe lupanga kapena mkondo
m’dzanja la aliyense amene anatsatira Saulo ndi Yonatani. Koma Saulo
ndi Yonatani, iwo okha ndiwo anali ndi zida.

*Yonatani Athira Nkhondo Afilisti*

23 Tsono gulu lina lankhondo la Chifilisti linapita kukalonda mpata wa
Mikimasi.

# 14

1 Tsiku lina Yonatani mwana wa Sauli anawuza mnyamata wake
womunyamulira zida zake za nkhondo kuti, “Tiye tiwoloke tipite ku
kaboma ka Afilisti tsidya ilo.” Koma iye sanawuze abambo ake.

2 Sauli ankakhala m’malire a Gibeya pa tsinde pa mtengo wamakan-
gadza ku Migironi. Anthu amene anali naye analipo 600. 3 Pakati pawo
panalinso Ahiya amene ankavala efodi. Iye anali mwana wa Ahitubi,
m’bale wake wa Ikabodi mwana wa Finehasi, mwana wa Eli, wansembe

wa Yehova wa ku Silo. Koma palibe amene anadziwa kuti Yonatani
wachoka.
4 Pa mpata pamene Yonatani ankafuna kudutsa kukafika ku kaboma
ka nkhondo ka Afilisti kunali thanthwe lotsetsereka mbali ina ndi
lina lotsetsereka mbali inayo. Thanthwe limodzi linkatchedwa Bozezi
ndipo linalo linkatchedwa Seni. 5 Thanthwe limodzi linali chakumpoto
kuyang'anana ndi Mikimasi, ndipo thanthwe linalo linali chakummwera
kuyang'anana ndi Geba.
6 Yonatani anawuza mnyamata wake womunyamulira zida uja kuti,
"Tiye tiwoloke tipite ku kaboma ka anthu osachita mdulidwewo. Mwina
Yehova adzatigwirira ntchito. Palibe chomuletsa Yehova kutipulumutsa,
ngakhale tikhale ambiri kapena ochepa."
7 Mnyamata uja anati, "Chitani chilichonse chimene mtima wanu
ukhumba. Ine ndili nanu pamodzi. Chimene mtima wanu ukhumba ndi
chomwenso ine ndikhumba."
8 Yonatani anati, "Tiye tsono tiwoloke kupita kumene kuli anthuwo ndi
kukadzionetsa kwa iwo. 9 Akatiwuza kuti, 'Imani pomwepo mpaka tiku-
pezeni,' ife tikangoyima pomwepo osapita kumene kuli iwoko. 10 Koma
akadzati, 'Bwerani kuno,' ndiye ife tikapitedi, chifukwa ichi chidzakhala
chizindikiro chakuti Yehova wapereka m'manja mwathu."
11 Choncho awiriwa anadzionetsa ku kaboma ka nkhondo ka Afilisti.
Tsono Afilistiwo anati, "Taonani! Aheberi akutuluka m'maenje m'mene
anabisala." 12 Anthu a ku kaboma kaja anafuwula kwa Yonatani
ndi mnyamata wake uja kuti, "Bwerani kuno ndipo tikuphunzitsani
phunziro."
Ndipo Yonatani anati kwa mnyamata wake. "Nditsate pakuti Yehova
wapereka Afilistiwa m'manja mwa Aisraeli."
13 Choncho Yonatani anakwera mokwawa, ndipo mnyamata wake
uja ankamutsata. Tsono Yonatani anathira nkhondo Afilisti aja na-
mawagwetsa, ndipo mnyamata wake uja ankawapha pambuyo pa iyeyo.
14 Nthawi yoyambayo Yonatani ndi mnyamata wake uja anapha anthu
makumi awiri ndipo anawaphera pa malo ochepa okwanira ngati theka
la ekala.

### *Aisraeli Agonjetsa Afilisti*

15 Tsono gulu lonse la ankhondo, ndiye kuti iwo amene anali m'misasa
ndi m'minda ndiponso iwo amene anali ku kaboma ka ankhondo kaja,
onse anagwidwa ndi mantha aakulu. Dzikonso linagwedezeka, choncho
anthu anachita mantha koopsa.
16 Alonda a Sauli a ku Gibeya dziko la Benjamini atangomwaza maso
anangoona chigulu cha asilikali chikumwazikana uku ndi uku. 17 Kenaka
Sauli anawawuza anthu amene anali naye kuti, "Awerengeni asilikali
kuti muona amene wachoka." Atawawerenga anapeza kuti Yonatani ndi
mnyamata wake womunyamulira zida zake za nkhondo palibe.
18 Tsono Sauli anawuza Ahiya kuti, "Bwera nalo Bokosi la Mulungulo."
(Nthawi imeneyo n'kuti efodiyo ili ndi Ahiya pamaso pa Aisraeli).
19 Pamene Sauli amayankhula ndi wansembe, phokoso limanka likuli-
rakulira mu msasa wa Afilisti, Kotero Sauli anati kwa wansembe, "Leka
kuwombeza."
20 Ndipo Sauli ndi asilikali onse amene anali naye anasonkhana
kupita kukamenya nkhondo, ndipo anangoona chisokonezo chachikulu
kwambiri. Afilisti akuphana okhaokha. 21 Aheberi ena amene kale anali

ndi Afilisti mpaka kukakhala ku misasa yawo, iwonso anatembenuka nakhala pamodzi ndi Aisraeli amene ankatsata Sauli ndi Yonatani.
22 Ngakhale Aisraeli amene ankabisala ku dziko lamapiri la Efereimu atamva kuti Afilisti akuthawa, nawonso anawathamangitsa Afilistiwo nawathira nkhondo. 23 Nkhondo inapitirira mpaka kufika ku Beti-Aveni.
Choncho Yehova anapulumutsa Aisraeli tsiku limenelo.

### *Yonatani Adya Uchi*

24 Koma asilikali a Israeli anavutika tsiku limenelo, chifukwa Sauli anawalumbirira Aisraeli kuti, "Wotembereredwa munthu aliyense amene adzadya kusanade, ine ndisanalipsire adani anga!" Kotero palibe wankhondo aliyense amene analawa chakudya.

25 Gulu lonse la ankhondo linalowa m'nkhalango mmene munali uchi.
26 Atalowa m'nkhalango, anaona uchi ukukha, koma palibe amene anadya, pakuti ankaopa lumbiro lija. 27 Koma Yonatani sanamve kuti abambo ake anawalumbirira anthu aja choncho anatenga ndodo yake imene inali m'dzanja lake ndipo anayipisa mu chisa cha njuchi. Choncho iye anadya uchiwo ndipo m'maso mwake munayera. 28 Kenaka mmodzi mwa Asilikali anamuwuza kuti, "Abambo ako alumbirira anthu nati, 'Wotembereredwa munthu aliyense amene adye chakudya lero.' N'chifukwa chake anthu alefuka."

29 Yonatani anati, "Abambo anga achita chinthu choyipira dziko. Taonani m'maso mwanga mwayera chifukwa ndalawa uchiwu pang'ono.
30 Zikanakhala zabwino kwambiri anthuwa akanadya lero zofunkha za adani awo. Zikanatero tikanapha Afilisti ochuluka."

31 Tsiku limenelo Aisraeli anapha Afilisti kuchokera ku Mikimasi mpaka ku Ayaloni. Koma Aisraeliwo analefuka kwambiri ndi njala. 32 Choncho iwo anathamangira pa zofunkha ndipo anatenga nkhosa, ng'ombe ndi ana ang'ombe. Iwo anazipha zonsezi nazidya pamodzi ndi magazi omwe.
33 Koma anthu ena anawuza Sauli kuti, "Taona anthu akuchimwira Yehova pakudya nyama yomwe ili ndi magazi."

Ndipo Sauli anati, "Mwaonetsa kusakhulupirika. Tsopano gubuduzirani mwala waukulu pano." 34 Kenaka Sauli anati, "Mwazikanani pakati pa anthu ndi kukawawuza kuti aliyense abwere ndi ng'ombe yake kapena nkhosa yake, ndipo adzayiphe pomwe pano ndi kuyidya. Musachimwire Yehova pakudya nyama imene ili ndi magazi."

Kotero aliyense anabwera ndi ng'ombe yake usiku womwewo ndi kuyipha pomwepo. 35 Ndipo Sauli anamangira Yehova guwa. Ili linali guwa loyamba limene Sauli anamangira Yehova.

36 Sauli anati, "Tiyeni titsatire Afilisti usikuwu ndi kulanda zinthu zawo mpaka mmawa. Tisasiyepo wamoyo ndi mmodzi yemwe."

Ankhondowo anayankha kuti, "Chitani chilichonse chimene chikukomerani."

Koma wansembe anati, "Tipemphe uphungu kwa Mulungu poyamba."

37 Choncho Sauli anafunsa Mulungu kuti, "Kodi ndiwatsatire Afilisti? Kodi mukawapereka m'manja mwathu?" Koma Mulungu sanamuyankhe tsiku limenelo.

38 Choncho Sauli anati, "Bwerani kuno nonse atsogoleri a anthu, ndipo tiyeni tione kuti kodi tchimo limeneli lachitika bwanji lero? 39 Pali Yehova amene amapulumutsa Israeli, ngakhale tchimolo litapezeka ndi mwana wanga Yonatani, iye afe ndithu." Koma palibe ndi mmodzi yemwe mwa anthuwo amene anamuyankha.

40 Tsono Sauli anawuza Aisraeli onse kuti, “Inu mukhale mbali imodzi.
Ine ndi mwana wanga Yonatani tikhala mbali inayo.”

“Chitani chilichonse chimene chikukomerani.”

41 Ndipo Sauli anapemphera kwa Yehova Mulungu wa Israeli kuti,
“Chifukwa chiyani simunandiyankhe ine mtumiki wanu lero lino? Ngati
tchimoli lipezeka ndi ine kapena ndi Yonatani mwana wanga, Inu
Mulungu wa Israeli, aoneke ndi Urimu. Koma ngati wochimwa ndi anthu
anu, Aisraeli aoneke Tamimu.” Maere anagwera Sauli ndi Yonatani ndipo
anthu anapezeka osalakwa. 42 Sauli anati, “Chitani maere pakati pa ine
ndi Yonatani mwana wanga.” Ndipo maere anagwera Yonatani.

43 Kenaka Sauli anati kwa Yonatani, “Ndiwuze chimene wachita.”

Ndipo Yonatani anamuwuza kuti, “Ine ndinangolawa uchi pang’ono ndi
ndodo yangayi. Ndiye ine ndili wokonzeka kufa.”

44 Sauli anati, “Mulungu andilange ngakhale kufa kumene, ngati sufa
iwe Yonatani.”

45 Koma anthuwo anafunsa Saulo kuti, “Kodi Yonatani afe, iye amene
wagwira ntchito iyi yayikulu yopulumutsa Aisraeli? Osatheka! Pali Yehova
ngakhale tsitsi ndi limodzi lomwe lapamutu pake silidzathothoka, pakuti
wachita zimenezi lero ndi thandizo la Mulungu.” Choncho anthuwo
anamupulumutsa Yonatani, ndipo sanaphedwe.

46 Pambuyo pake Sauli analeka kulondola Afilisti, kenaka anabwerera
ku dziko lawo.

47 Sauli ali mtsogoleri wa Israeli, anachita nkhondo ndi adani awa
omuzungulira: Mowabu, Amoni, Edomu mafumu a ku Zoba ndi Afilisti.
Kulikonse kumene ankapita ankawagonjetsa. 48 Anachita nkhondo
mwamphamvu ndi kugonjetsa Aamaleki. Choncho anapulumutsa Aisraeli
m’manja mwa anthu amene ankawalanda zinthu zawo.

### *Banja la Sauli*

49 Ana aamuna a Sauli anali Yonatani, Isivi ndi Maliki-Suwa. Analinso
ndi ana aakazi awiri, dzina la mwana wake wamkulu wamkazi linali
Merabi ndipo la mwana wake wamng’ono wamkazi linali Mikala. 50 Dzina
la mkazi wake linali Ahinoamu. Iyeyu anali mwana wa Ahimaazi. Dzina
la mkulu wa ankhondo a Sauli linali Abineri mwana wa Neri, m’bale wa
abambo a Sauli. 51 Kisi abambo a Sauli ndi Neri abambo a Abineri anali
ana a Abieli.

52 Pa moyo wake wonse, Sauli ankakhalira kuchita nkhondo pakati
pa Israeli ndi Afilisti. Ndipo Sauli ankati akaona munthu aliyense
wamphamvu kapena wolimba mtima ankamulemba ntchito mu gulu lake
lankhondo.

## 15

### *Yehova Akana Sauli Kukhala Mfumu*

1 Samueli anawuza Sauli kuti, “Yehova ananditumа ine kuti ndikud-
zozeni kukhala mfumu ya anthu ake, Aisraeli. Tsopano imvani zimene
Yehova akunena. 2 Yehova Wamphamvuzonse akuti, ‘Ine ndidzalanga
Aamaleki chifukwa cha zimene anawachita Aisraeli. Paja iwo analimbana
ndi Aisraeli pa njira pamene Aisraeliwo ankachoka ku Igupto. 3 Tsopano
pita kathire nkhondo Aamaleki ndi kuwononga kwathunthu zinthu zonse
zimene ali nazo. Musakasiyeko munthu ndi mmodzi yemwe. Mukaphe
amuna ndi akazi, ana ndi makanda, ng’ombe ndi nkhosa, ngamira ndi
abulu.’ ”

4 Kotero Sauli anayitana ankhondo ake nawawerenga ku Telaimu.
Ankhondo oyenda pansi analipo 200,000 ndipo mwa iwowa 10,000 anali
a fuko la Yuda. 5 Sauli anapita ku mzinda wa Aamaleki nawubisalira
m'khwawa. 6 Tsono Sauli anawuza Akeni kuti, "Samukani, muchoke
pakati pa Aamaleki kuti ine ndisakuwonongeni pamodzi ndi iwo pakuti
inu munaonetsa kukoma mtima kwa Aisraeli onse pamene ankatuluka
m'dziko la Igupto," Choncho Akeni anachoka pakati pa Aamaleki.
7 Tsono Sauli anakantha Aamaleki kuchokera ku Havila mpaka ku Suri,
kummawa kwa Igupto. 8 Sauli anatenga Agagi mfumu ya Aamaleki, koma
anthu ake onse anawapha ndi lupanga. 9 Koma Sauli ndi ankhondo ake
sanaphe Agagi, sanaphenso nkhosa ndi ng'ombe zabwino ngakhalenso
ana ang'ombe ndi ana ankhosa onenepa. Chilichonse chimene chinali
chabwino sanachiphe. Koma zonse zimene zinali zoyipa ndi zachabechabe
anaziwononga.
10 Kenaka Yehova anawuza Samueli kuti, 11 "Ine ndikumva chisoni
chifukwa ndinayika Sauli kukhala mfumu. Wabwerera m'mbuyo, waleka
kunditsata ndipo sanamvere malangizo anga." Samueli anapsa mtima,
ndipo analira kwa Yehova usiku wonse.
12 Samueli anadzuka mmamawa ndipo anapita kukakumana ndi Sauli.
Koma anthu anamuwuza kuti, "Sauli anabwera ku Karimeli, ndipo
kumeneko wadziyimikira mwala wachikumbutso cha iye mwini. Tsopano
wachokako ndipo wapita ku Giligala."
13 Samueli atamupeza Sauli, Sauliyo anati kwa Samueli, "Yehova
akudalitseni! Ndachita zonse zimene Yehova analamula."
14 Koma Samueli anati, "Nanga bwanji ndikumva kulira kwa nkhosa ndi
ng'ombe?"
15 Sauli anayankha, "Zimenezi Asilikali azitenga kuchokera kwa Aa-
maleki. Iwo anasungako nkhosa ndi ng'ombe zabwino kuti akapereke
nsembe kwa Yehova Mulungu wanu, koma zina zonse anaziwononga."
16 Koma Samueli anati kwa Sauli, "Khala chete! Ima ndikuwuze zimene
Yehova wandiwuza usiku wathawu."
Sauli anayankha kuti, "Ndiwuzeni."
17 Apo Samueli anati, "Munali wamng'ono pa maso pa anthu, koma
tsopano mwasanduka mtsogoleri wa mafuko a Israeli. Yehova anakud-
zozani kuti mukhale mfumu yolamulira Aisraeli. 18 Ndipo Yehova anaku-
tumani kuti, 'Pitani mukawononge kwathunthu Aamaleki, anthu oyipa
aja. Mukachite nawo nkhondo mpaka kuwatheratu.' 19 Chifukwa chiyani
simunamvere mawu a Yehova? Chifukwa chiyani munathamangira
zofunkha ndi kuchita choyipira Yehova?"
20 Koma Saulo anawuza Samueli kuti, "Ine ndinamveradi mawu a
Yehova. Ndinapita kukachita zimene Yehova ananditumа. Ndinabwera
naye Agagi, mfumu ya Amaleki, koma Aamaleki ena onse anaphedwa.
21 Koma pa zofunkhazo anthu anatengapo nkhosa, ng'ombe ndi zabwino
zina zoyenera kuwonongedwa kuti akapereke ngati nsembe kwa Yehova
Mulungu wanu ku Giligala."
22 Koma Samueli anayankha kuti,
"Kodi Yehova amakondwera ndi nsembe zopsereza ndi nsembe zina
kapena kumvera mawu a ake?
Taona, kumvera ndi kwabwino kuposa nsembe,
ndipo kutchera khutu ndi kwabwino kuposa kupereka mafuta a
nkhosa.
23 Pakuti kuwukira kuli ngati tchimo lowombeza,

ndipo kukhala nkhutukumve kuli ngati tchimo lopembedza mafano.
Chifukwa mwakana mawu a Yehova.
Iyenso wakukana kuti iweyo ukhale mfumu."
24 Tsono Sauli anati kwa Samueli, "Ine ndachimwa. Ndaphwanya
malamulo a Yehova ndiponso malangizo anu. Ndinkaopa anthu ndipo
ndinawamvera. 25 Tsopano ndikukupemphani, khululukireni tchimo
langa ndipo mubwerere nane kuti ndikapembedze Yehova."
26 Koma Samueli anawuza Sauli kuti, "Ine sindibwerera nawe. Inu
mwakana mawu a Yehova. Choncho Iyenso wakukanani kuti musakhale
mfumu yolamulira Aisraeli."
27 Samueli akutembenuka kuti azipita, Sauli anagwira mpendero wa
mkanjo wake, ndipo unang'ambika. 28 Samueli anati kwa iye, "Yehova
wang'amba ufumu wanu kuchoka kwa inu, ndipo waupereka kwa
mnzanu woposa inu. 29 Mulungu wa ulemerero wa Israeli sanama kapena
kusintha maganizo ake; pakuti iye si munthu, kuti asinthe maganizo ake."
30 Sauli anati, "Ine ndachimwa. Komabe, chonde mundilemekeze pa-
maso pa akuluakulu, anthu anga, ndiponso pamaso pa Israeli. Mubwerere
nane kuti ndikapembedze Yehova Mulungu wanu." 31 Pamenepo Samueli
anabwerera ndi Sauli, ndipo Sauli anapembedza Yehova.
32 Kenaka Samueli anati, "Bwera nayeni kuno Agagi, mfumu ya Amaleki
ija."
Choncho Agagi anapita kwa Samueli mokondwa chifukwa ankaganiza
kuti, "Ndithu zowawa za imfa zapita."
33 Koma Samueli anati,
"Monga momwe lupanga lako linasandutsira amayi kukhala wopanda ana,
momwemonso amayi ako adzakhala opanda mwana pakati pa amayi."
Ndipo Samueli anapha Agagi pamaso pa Yehova ku Giligala.
34 Ndipo Samueli anapita ku Rama, koma Sauli anapita ku mudzi kwawo
ku Gibeya wa Sauli. 35 Samueli sanamuonenso Sauli mpaka imfa yake
ngakhale kuti ankamulira Sauliyo. Yehova anamva chisoni kuti anasankha
Sauli kuti akhale mfumu ya Israeli.

# 16

*Samueli Adzoza Davide Kukhala Mfumu*

1 Yehova anati kwa Samueli, "Kodi udzamulira Sauli mpaka liti,
popeza Ine ndamukana kuti akhale mfumu ya Israeli? Dzaza mafuta
m'botolo lako ndipo unyamuke kupita kwa Yese wa ku Betelehemu popeza
ndadzisankhira mmodzi mwa ana ake kukhala mfumu."
2 Koma Samueli anati, "Kodi ndingapite bwanji? Sauli akamva zimenezi
adzandipha."
Yehova anayankha, "Tenga ng'ombe yayikazi ndipo ukanene kuti,
'Ndabwera kudzapereka nsembe kwa Yehova. 3 Ukamuyitane Yese ku
mwambo wa nsembe, ndipo ine ndidzakuwuza choti ukachite. Ukandid-
zozere amene ndikakulozere.' "
4 Samueli anachita zimene Yehova ananena, ndipo anabweradi ku
Betelehemu kuja. Akuluakulu a mu mzindawo anamuchingamira ali
njenjenje ndi mantha ndipo anamufunsa kuti, "Kodi mwabwera mwa
mtendere?"
5 Samueli anayankha kuti, "Inde, kwabwino. Ndabwera kudzapereka
nsembe kwa Yehova. Mudzipatule ndipo mubwere kudzapereka nsembe

pamodzi nane.” Kenaka iye anamupatula Yese ndi ana ake aamuna ndipo
anawayitana kudzapereka nsembe.

6 Pamene anafika, Samueli anaona Eliabu ndipo anaganiza “Ndithu
wodzozedwa wa Yehova uja ndi uyu wayima pamaso pakeyu.”

7 Koma Yehova anati kwa Samueli, “Usaone maonekedwe ake kapena
msinkhu wake, pakuti ndamukana iyeyu. Yehova sapenya zimene munthu
amapenya. Anthu amapenya zakunja, koma Mulungu amapenya za mu
mtima.”

8 Kenaka Yese anayitana Abinadabu namubweretsa pamaso pa Samueli.
Koma Samueli anati, “Yehova sanamusankhenso ameneyu.” 9 Ndipo Yese
anayitana Sama, koma Samueli anati, “Ngakhale uyu Yehova sanamu-
sankhe.” 10 Pambuyo pake, Yese anayitana ana ake amuna asanu ndi
awiri kuti apite kwa Samueli. Koma Samueli anati, “Yehova sanasankhe
amenewa.” 11 Tsono Samueli anafunsa Yese kuti, “Kodi awa ndi ana ako
onse aamuna?”

Yese anayankha kuti, “Ayi, alipo wina wamng’ono amene watsala, koma
akuweta nkhosa.”

Samueli anati, “Apite munthu akamutenge popeza sitipereka nsembe
mpaka iye atabwera.”

12 Choncho anatuma munthu kukamutenga ndipo anabwera naye. Iye
anali wofiirira, wa maonekedwe abwino ochititsa kaso.

Ndipo Yehova anati, “Mudzoze popeza ndi ameneyu.”

13 Samueli anatenga botolo la mafuta ndi kumudzoza pamaso pa
abale ake, ndipo Mzimu wa Yehova unabwera mwamphamvu pa Davide
kuyambira tsiku limenelo mpaka m’tsogolo. Pambuyo pake Samueli
anabwerera ku Rama.

### *Davide Atumikira Sauli*

14 Nthawi imeneyo Mzimu wa Yehova unamuchokera Sauli, ndipo
mzimu woyipa wochokera kwa Yehova unayamba kumuzunza.

15 Atumiki a Sauli anati, “Taonani mzimu woyipa wochokera kwa Mu-
lungu ukukuzunzani. 16 Ndiyetu, inu mbuye wathu titumeni ife antchito
anu kuti tikafune munthu wodziwa bwino kuyimba zeze. Tsono pamene
mzimu woyipa wochokera kwa Mulungu wakufikirani, iye azidzayimba
ndipo mudzakhala bwino.”

17 Choncho Sauli anati kwa atumiki ake, “Chabwino, kandipezereni
munthu wodziwa bwino kuyimba ndipo mubwere naye kuno.”

18 Mmodzi mwa antchito ake anati, “Ine ndinaona mwana wa Yese
wa ku Betelehemu. Ndiye munthu wodziwa bwino kuyimba, wolimba
mtima, ngwazi pa nkhondo, wodziwa kuyankhula ndi wokongola. Ndipotu
Yehova ali ndi iye.”

19 Ndipo Sauli anatumiza amithenga kwa Yese kukanena kuti, “Ndi-
tumizireni mwana wanu Davide, amene amaweta nkhosa.” 20 Choncho
Yese anatenga bulu namunyamulitsa buledi, thumba la vinyo ndi mwana
wambuzi mmodzi. Zonsezi anamupatsa mwana wake Davide kuti
akapereke kwa Sauli.

21 Davide anafika kwa Sauli ndipo anayamba ntchito. Sauli ana-
mukonda kwambiri Davide ndipo anamusandutsa wonyamula zida zake
za nkhondo. 22 Kenaka Sauli anatumiza mawu kwa Yese ndi kuti, “Mulole
kuti Davide azinditumikira, pakuti ndamukonda kwambiri.”

23 Nthawi zonse mzimu woyipa wochokera kwa Mulungu umati uka-
mufikira Sauli, Davide ankatenga zeze wake n'kumamuyimbira. Choncho
Sauli ankapeza bwino, ndipo mzimu woyipa uja unkamusiya.

# 17

*Davide ndi Goliati*

1 Afilisti anasonkhanitsa ankhondo awo ku Soko m'dziko la Yuda. Iwo
anamanga misasa yawo ku Efesi-Damimu, pakati pa Soko ndi Azeka.
2 Sauli ndi Aisraeli anasonkhana namanga misasa m'chigwa cha Ela ndipo
anandandalitsa ankhondo kuti amenyane ndi Afilisti. 3 Afilisti anali phiri
lina ndipo Aisraeli analinso phiri lina, ndipo pakati pawo panali chigwa.

4 Tsono munthu wina wamphamvu, dzina lake Goliati wochokera ku
Gati anatuluka ku misasa ya Afilisti. Msinkhu wake unali pafupipafupi
mamita atatu. 5 Iye ankavala chipewa chamkuwa ndi malaya achitsulo
olemera makilogalamu 57. 6 Ankavalanso zokuta miyendo yake zamkuwa,
ndipo ankanyamula nthungo ya mkuwa pa phewa pake. 7 Thunthu la
mkondo wake linali ngati mkombero wowombera nsalu, ndipo mutu wa
mkondowo unkalemera makilogalamu asanu ndi awiri. Patsogolo pake
pamakhala munthu wonyamula zida zake za nkhondo.

8 Goliatiyo anayimirira ndi kufuwula kwa ankhondo a Israeli, nati,
"N'chifukwa chiyani mwakonzekera nkhondo chotere? Kodi sindine
Mfilisiti ndipo inu sindinu akapolo a Sauli? Sankhani munthu kuti
abwere kwa ine. 9 Ngati angathe kumenyana nane ndi kundipha, ife
tidzakhala akapolo anu, koma ngati ine ndimugonjetsa ndi kumupha,
inu mudzakhala akapolo athu ndi kumatitumikira." 10 Ndipo Mfilisitiyo
anati, "Bwerani lero timenyane basi! Patseni munthu kuti ndimenyane
naye." 11 Atamva mawu a Mfilisitiyo, Sauli ndi Aisraeli onse anataya
mtima nachita mantha kwambiri.

12 Davide anali mwana wa munthu wa fuko la Efurati dzina lake Yese
amene amachokera ku Betelehemu m'dziko la Yuda. Yese anali ndi ana
aamuna asanu ndi awiri. Pa nthawi ya Sauli n'kuti ali wokalamba. 13 Ana
atatu oyamba kubadwa a Yese n'kuti atapita nawo ku nkhondo pamodzi
ndi Sauli. Woyamba dzina lake anali Eliabu, wachiwiri anali Abinadabu,
ndipo wachitatu anali Sama. 14 Davide ndiye anali mzime. Ana aakulu
atatuwo ndiwo anapita ku nkhondo ndi Sauli. 15 Koma Davide ankapita
ku misasa ya Sauli ndi kubwerako kuti azikaweta nkhosa za abambo ake
ku Betelehemu.

16 Kwa masiku makumi anayi, Mfilisiti uja ankabwera mmawa ndi
madzulo kumadzionetsera.

17 Tsiku lina Yese anawuza mwana wake Davide kuti, "Atengere abale
ako makilogalamu khumi a tirigu wokazinga ndi malofu a buledi khumi
ndipo upite nazo mofulumira ku misasa yawo. 18 Utengerenso wolamulira
wa gulu lawo tchizi khumi uyu. Ukaone mmene abale ako akukhalira
ndipo ubwere ndi kanthu kosonyeza kuti ali bwino. 19 Sauli, abale akowo
ndi asilikali onse a Israeli ali ku chigwa cha Ela, akumenyana ndi Afilisti."

20 M'mamawa mwake Davide anasiya nkhosa m'manja mwa munthu
wina ndipo anatenga zakudyazo nanyamuka monga momwe Yese abambo
ake anamulamulira. Anakafika ku misasa pamene asilikali ankapita
kukandanda pa mzere ku nkhondo, n'kufuwula mfuwu wankhondo.
21 Aisraeli ndi Afilisti anandanda pa mzere wankhondo moyang'anana.
22 Tsono Davide anasiyira zakudya zija munthu wosunga katundu

nathamangira kumene kunali ankhondo kuja ndi kukalonjera abale ake.
23 Pamene iye ankayankhula nawo anangoona Goliati wa ku Gati uja
akuchoka pa mzere wa Afilisti akufuwula mawu onyoza monga mwa
masiku onse, ndipo Davide ankawamva. 24 Aisraeli ataona munthuyo,
anamuthawa ndi mantha aakulu.

25 Ndipo Aisraeli ankanena kuti, "Kodi mwamuona munthu akubwer-
ayo? Iye amangobwera kudzanyoza Israeli. Tsono mfumu inati kuti idza-
pereka chuma chambiri kwa munthu amene adzamuphe. Idzaperekanso
mwana wake wamkazi kuti amukwatire ndiponso banja la abambo ake
silidzaperekanso msonkho mu Israeli."

26 Davide anafunsa anthu amene anayima pafupi naye kuti, "Kodi
adzamuchita chiyani munthu amene adzapha Mfilisiti uyu ndi kuchotsa
chitonzo pakati pa Israeli? Mfilisiti wosachita mdulidweyu ndi ndani kuti
azinyoza gulu lankhondo la Mulungu wamoyo?"

27 Anthu anamuwuzanso zonse zimene mfumu inanena kuti idzachitira
munthu amene adzapha Mfilisitiyo.

28 Eliabu, mkulu wake wa Davide, atamumva akuyankhula ndi anthuwo,
anamukwiyira ndipo anamufunsa kuti, "N'chifukwa chiyani wabwera
kuno? Ndipo wasiyira yani nkhosa zochepazo m'chipululu? Ndikudziwa
kuti ndiwe wodzikuza ndiponso woyipa mtima. Unabwera kuno kuti
udzaonere nkhondo."

29 Davide anati, "Kodi ndachita chiyani ine? Kodi ndisamayankhule?"
30 Ndipo anamuchokera napita kwa munthu wina ndipo anamufunsa
nkhani yomweyo, ndipo anthu anamuyankha iye monga poyamba paja.
31 Mawu amene Davide anayankhula atamveka, anthu anakafotokozera
Sauli ndipo Sauli anamuyitanitsa.

32 Davide anati kwa Sauli, "Munthu aliyense asataye mtima chifukwa
cha Mfilisitiyu. Ine kapolo wanu ndipita kukamenyana naye."

33 Sauli anayankha Davide kuti, "Iwe sungathe kupita kukamenyana
ndi Mfilisitiyu. Iwe ukanali mnyamata, koma iyeyu ndi amene wakhala
akumenya nkhondo kuyambira unyamata wake."

34 Koma Davide anati kwa Sauli, "Kapolo wanune ndinkaweta nkhosa
za abambo anga. Ndipo mkango kapena chimbalangondo chikamabwera
ndi kugwira mwana wankhosa pakati pa nkhosazo, 35 ine ndinkatsatira
ndi kupha chirombocho. Choncho ndinkapulumutsa mwana wankhosa
uja m'kamwa mwake. Ndipo chinkati chikandiwukira, ine ndinkagwira
tchowa lake, n'kuchikantha mpaka kuchipha. 36 Ine kapolo wanu ndi-
napha mkango ngakhalenso chimbalangondo. Tsono Mfilisiti wosachita
mdulidweyu adzaphedwa monga zinazo chifukwa wanyoza ankhondo
a Mulungu wamoyo. 37 Yehova amene anandilanditsa m'kamwa mwa
mkango ndi chimbalangondo adzandilanditsa m'manja mwa Mfilisiti
uyu."

Sauli anati kwa Davide, "Pita, ndipo Yehova akhale nawe."

38 Ndipo Sauli anamveka Davide mwinjiro wake. Anamuveka zovala
zankhondo ndi chipewa cha mkuwa. 39 Davide anamangirira lupanga
pa mwinjirowo. Atayesa kuyenda nazo, analephera chifukwa anali
asanazizolowere.

Iye anati kwa Sauli, "Sindingathe kuyenda nazo chifukwa sindinazi-
zolowere." Ndipo anazivula. 40 Pambuyo pake anatenga ndodo yake
m'manja. Kenaka anasankha miyala yosalala bwino mu mtsinje ndi

kuyiika m'thumba lake la ku ubusa. Legeni ili m'manja mwake, Davide
ananyamuka kukakumana ndi Mfilisiti uja.

41 Tsono Mfilisiti uja anayambapo kupita kumene kunali Davide, mnya-
mata wonyamula zida zake za nkhondo ali patsogolo pake. 42 Mfilisitiyo
atangomuona Davide, anamunyoza popeza kuti Davide anali mnyamata
chabe wofiirira ndi wa maonekedwe abwino. 43 Iye anati kwa Davide,
"Kodi ndine galu, kuti ubwere kwa ine ndi ndodo?" Ndipo Mfilisitiyo
anamutemberera Davide potchula mayina a milungu yake. 44 Iye
anatinso, "Bwera kuno ndipo ndidzapereka mnofu wako kwa mbalame
zamlengalenga ndi kwa zirombo zakuthengo!"

45 Koma Davide anati kwa Mfilisitiyo, "Iwe wabwera kwa ine ndi
lupanga, mkondo ndi nthungo, koma ine ndikubwera kwa iwe m'dzina
la Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa ankhondo Aisraeli amene
iwe ukuwanyoza. 46 Anatinso lero lino Yehova adzakupereka m'manja
mwanga. Ndidzakukantha ndi kudula mutu wako. Ndidzapereka
mitembo ya asilikali a Afilisti kwa mbalame za mlengalenga, ndi kwa
zirombo zakuthengo ndipo dziko lonse lapansi lidzadziwa kuti mu Israeli
muli Mulungu. 47 Onse amene asonkhana pano adzadziwa kuti Mulungu
sapulumutsa anthu ndi lupanga kapena mkondo, pakuti nkhondo ndi ya
Yehova. Iye adzakuperekani m'manja mwathu."

48 Mfilisitiyo akusendera pafupi kuti akumane naye, Davideyo
anathamangira mofulumira ku mzere wa nkhondo kukakumana naye.
49 Davideyo anapisa dzanja lake m'thumba lake natengamo mwala ndipo
anawuponya, nalasa pa mphumi pa Mfilisitiyo. Mwalawo unalowa pa
chipumi chake, ndipo anagwa chafufumimba.

50 Kotero Davide anamupambana Mfilisitiyo pomugenda ndi mwala wa
legeni ndi kumupha. M'manja mwa Davide munalibe lupanga.

51 Davide anathamanga nakayimirira pamwamba pa Mfilisiti uja. Ana-
sosola lupanga lake lomwe moyikamo mwake, namupha pomudula mutu
wake.

Afilisti ataona kuti ngwazi yawo yafa, anathawa. 52 Ndipo Aisraeli ndi
anthu a ku Yuda ananyamuka, ndipo akufuwula anathamangitsa Afilisti
aja mpaka ku Gati ndi ku zipata za Ekroni. Anthu akufa awo amagwa
njira yonse ya ku Saaraimu mpaka ku Gati ndi ku Ekroni. 53 Aisraeli
anabwerako kothamangitsa Afilisti kuja ndipo anadzatenga zonse zimene
zinali m'misasa ya Afilistiwo. 54 Pambuyo pake Davide anatenga mutu wa
Mfilisitiyo napita nawo ku Yerusalemu, koma anayika zida za Mfilisitiyo
mu tenti yake.

55 Sauli ataona Davide akupita kukakumana ndi Mfilisitiyo anafunsa
Abineri, mkulu wa ankhondo kuti, "Abineri, kodi mnyamatayu ndi mwana
wa yani?"

Abineri anayankha kuti, "Ndithu mfumu muli apa ine sindikumudziwa."

56 Mfumu inati, "Pita kafufuze kuti mnyamata ameneyu ndi mwana wa
yani."

57 Davide atangobwerako kokapha Mfilisiti kuja, Abineri anamutenga
nabwera naye kwa Sauli, mutu wa Mfilisiti uja uli m'manja mwake.

58 Sauli anamufunsa, "Mnyamata iwe, kodi paja ndiwe mwana wayani?"

Davide anati, "Ndine mwana wa mtumiki wanu Yese wa ku Betele-
hemu."

# 18

### *Sauli Achitira Nsanje Davide*

1 Davide atatha kuyankhula ndi Sauli, mtima wa Yonatani unagwi-
rizana ndi mtima wa Davide, ndipo iye ankamukonda Davide monga
momwe ankadzikondera yekha. 2 Choncho Sauli anamusunga Davideyo
kuyambira tsiku limenelo ndipo sanamulole kuti abwerere ku nyumba ya
abambo ake. 3 Ndipo Yonatani anapanga pangano ndi Davide chifukwa
ankamukonda monga momwe ankadzikondera. 4 Yonatani anavula
mkanjo umene anavala ndipo anamupatsa Davide pamodzi ndi zovala za
nkhondo, lupanga, uta ndi lamba.

5 Davide ankapita kulikonse kumene Sauli ankamutuma kuti apite
kukamenya nkhondo, ndipo ankapambana. Choncho Sauli anamupatsa
udindo woyang'anira gulu lankhondo. Ichi chinakondweretsa anthu onse
ngakhalenso atsogoleri a nkhondo a Sauli.

6 Anthu akubwerera kwawo Davide atapha Mfilisiti uja, amayi anatuluka
m'mizinda yonse ya Israeli, akuyimba ndi kuvina kukachingamira mfumu
Sauli. Ankayimba ndi kuvina mokondwa, kwinaku ng'oma ndi zitoliro
zikulira. 7 Amayiwo ankalandizana nyimbo mokondwera namati:
"Sauli wapha 1,000,
Koma Davide wapha miyandamiyanda."

8 Koma Sauli anapsa mtima kwambiri ndipo mawu amenewa ana-
muyipira. Iye anati, "Iwo amuwerengera Davide miyandamiyanda, koma
ine 1,000 okha. Nanga chatsalanso n'chiyani kuti atenge? Si ufumu basi?"
9 Ndipo kuyambira tsiku limeneli Sauli ankamuchitira nsanje Davide.

10 Mmawa mwake mzimu woyipa uja unabwera mwamphamvu pa Sauli.
Sauli anayamba kubwebweta m'nyumba mwake. Davide ankamuyimbira
zeze monga nthawi zonse. Sauli anali ndi mkondo m'dzanja lake. 11 Tsono
anawuponya mkondowo, namati mu mtima mwake, "Ndimubaya Davide
ndi kumukhomera ku khoma." Koma Davide anawulewa kawiri konse.

12 Pambuyo pake Sauli amamuopa Davide chifukwa Yehova anali ndi
Davideyo, n'kumusiya Sauli. 13 Kotero Sauli anamuchotsa Davide pamaso
pake ndi kumuyika kukhala mtsogoleri wa ankhondo 1,000. Choncho
Davide ankapita ndi kubwera akutsogolera ankhondowa. 14 Davide anka-
pambana kwambiri pa chilichonse chimene amachita chifukwa Yehova
anali naye. 15 Sauli ataona momwe Davide ankapambanira, iye anamuopa
kwambiri. 16 Koma Aisraeli onse ndi anthu a Yuda ankamukonda Davide
chifukwa ankawatsogolera pa nkhondo zawo.

17 Tsiku lina Sauli anawuza Davide kuti, "Nayu Merabi mwana wanga
wamkazi wamkulu. Ine ndakupatsa kuti umukwatire. Koma unditumikire
molimba mtima pomenya nkhondo za Yehova." Poteropo Sauli ankanena
kuti, "Ndisamuphe ndi manja angawa koma aphedwe ndi Afilisti!"

18 Ndipo Davide anati kwa Sauli, "Ine ndine yani, ndipo abale anga
kapena banja la abambo anga ndife yani m'dziko la Israeli kuti ndikhale
mpongozi wa mfumu?" 19 Koma pa nthawi yoti Merabi mwana wa Sauli
akwatiwe ndi Davide, Sauli anamupereka kwa Adrieli wa ku Mehola kuti
amukwatire.

20 Koma Mikala mwana wamkazi wa Sauli anamukonda Davide ndipo
Sauli atamva za zimenezi, anakondwera. 21 Sauli ankaganiza kuti,
"Ndimupatse amukwatire kuti akhale ngati msampha kwa Davideyo,
ndipo adzaphedwe ndi Afilisti." Choncho Sauli anawuza Davide kachiwiri,
"Tsopano udzakhala mkamwini wanga."

22 Sauli analamulanso nduna zake kuti, “Muyankhuleni Davide
mwamseri ndi kumuwuza kuti, ‘Taona, mfumu imakondwera nawe, ndipo
nduna zake zonse zimakukonda. Tsono ukhale mkamwini wa mfumu.’ ”
23 Iwo anakamuwuza Davide mawu amenewa, koma Davide anati,
“Kodi inu mukuganiza kuti ndi chinthu chapafupi kukhala mpongozi wa
mfumu? Ine ndine wosauka ndiponso wosatchuka.”
24 Nduna za Sauli zinamuwuza zonse zimene anayankha Davide. 25 Sauli
anayankha kuti, “Kamuwuzeni Davide kuti, ‘Mfumu sikufuna malowolo a
mtundu wina uliwonse koma timakungu ta msonga za mavalo a Afilisti 100
kuti ilipsire adani ake.’ ” Maganizo a Sauli anali akuti Davide aphedwe ndi
Afilisti.
26 Nduna za Saulizo zitamuwuza Davide zimenezi, anakondwera kuti
akhale mpongozi wa mfumu. Koma nthawi imene anapatsidwa isanathe,
27 Davide ndi anyamata ake anapita ndi kukapha Afilisti 200. Iye anabwera
ndi timakungu tija natipereka tonse kwa mfumu kuti akhale mpongozi
wa mfumu. Kotero Sauli anapereka mwana wake wamkazi, Mikala, kwa
Davide kuti amukwatire.
28 Sauli atazindikira kuti Yehova anali ndi Davide ndiponso kuti mwana
wake Mikala amamukonda Davide, 29 iye anapitirirabe kumuopa Davide
ndi kumadana naye moyo wake wonse.
30 Nthawi zonse pamene atsogoleri a Afilisti ankatuluka kukamenya
nkhondo, Davide ankapambana kuposa nduna zonse za Sauli. Choncho
dzina lake linatchuka kwambiri.

# 19

### *Sauli Ayesanso Kupha Davide*

1 Sauli anawuza mwana wake Yonatani ndi nduna zake zonse kuti
aphe Davide. Koma Yonatani amamukonda kwambiri Davide. 2 Choncho
anawuza Davide kuti, “Abambo anga Sauli akufuna kukupha. Tsono
uchenjere. Mmawa upite ukabisale ndipo ukakhale komweko. 3 Ine
ndidzapita ndi kukayima pafupi ndi abambo anga ku munda kumene
iwe ukabisale. Ndipo ndidzayankhula ndi abambo anga za iwe ndipo
chilichonse chimene ndikamve ndidzakuwuza.”
4 Tsono Yonatani anakanena zabwino za Davide kwa abambo ake
Sauli ndipo anati, “Mfumu musachimwire mtumiki wanu Davide,
sanakuchimwireni, koma amakuchitirani zabwino kwambiri. 5 Iye
anayika moyo wake pa chiswe pamene anapha Mfilisiti uja. Choncho
Yehova anachita zazikulu popambanitsa Aisraeli pa nkhondo. Inu
munaona zonsezo ndipo munakondwera. Nanga n’chifukwa chiyani
mukufuna kuchimwira munthu wosalakwa pofuna kupha Davide?”
6 Sauli anamvera mawu a Yonatani ndipo analumbira kuti, “Pali Yehova,
Davide sadzaphedwa.”
7 Pambuyo pake Yonatani anayitana Davide namuwuza zonsezi. Chon-
cho Yonatani anabwera naye Davide kwa Sauli ndipo ankamutumikira
Sauliyo monga kale.
8 Panabukanso nkhondo ina ndipo Davide anapita ndi kukamenyana ndi
Afilisti. Iye anawakantha mwamphamvu kotero kuti Afilisti anathawa.
9 Tsiku lina mzimu woyipa uja unafikanso pa Sauli. Nthawi imeneyi
n’kuti Sauli uja ali m’nyumba mwake, mkondo uli m’dzanja lake ndi Da-
vide akuyimba zeze, 10 Sauli anafuna kumubaya Davide ndi kumukhomera

kukhoma, koma Davide anapewa mkondowo kotero Sauli anakabaya pa
khoma. Usiku womwewo Davide anathawa.
11 Usiku womwewo Sauli anatumiza anthu ku nyumba ya Davide kuti
akamubisalire ndi kumupha mmamawa. Koma Mikala mkazi wake
anamuchenjeza nati, "Ngati usiku uno supulumutsa moyo wako, mawa
udzaphedwa." 12 Choncho Mikala anamutulutsira Davide pa zenera, ndipo
anathawa ndi kupulumuka. 13 Kenaka Mikala anatenga fano naligoneka
pa bedi nayika pilo wa ubweya wa mbuzi ku mutu kwa fanolo ndipo
analifunditsa nsalu.
14 Pamene amithenga a Sauli aja anafika kuti akamugwire Davide,
Mikala anati, "Davide akudwala."
15 Koma Sauli anatumanso anthuwo kuti akamuone Davide, nati,
"Mubwere naye kuno ali pa bedi pomwepo kuti ndidzamuphe." 16 Koma
pamene anthuwo analowa, anangoona fano pa bedipo ndi pilo wa ubweya
wa mbuzi ku mutu kwake.
17 Tsono Sauli anafunsa Mikala kuti, "N'chifukwa chiyani wandinamiza
chotere polola kuti mdani wanga athawe?"
Mikala anayankha kuti, "Davide anandiwuza kuti, 'Ukapanda kutero
ndikupha.' "
18 Choncho Davide anathawa napulumuka. Pambuyo pake anapita kwa
Samueli ku Rama nakamuwuza zonse zimene Sauli anamuchita. Kenaka
iye ndi Samueli anapita kukakhala ku Nayoti. 19 Sauli anamva kuti,
"Davide ali ku Nayoti ku Rama." 20 Choncho iye anatumiza anthu kuti
akamugwire Davide. Koma anaona gulu la aneneri likulosera ndi Samueli
akuwatsogolera. Pomwepo Mzimu wa Mulungu unawafikira ndipo
nawonso anayamba kulosera. 21 Sauli atamva zimenezi anatumizanso
anthu ena, koma nawonso anayamba kulosa. Anatumanso anthu ena
kachitatu, koma nawonso anayamba kulosa. 22 Pomaliza Sauli mwini wake
ananyamuka kupita ku Rama ndipo anafika ku chitsime chachikulu cha
ku Seku. Ndipo anafunsa, "Samueli ndi Davide ali kuti?"
Munthu wina anamuyankha kuti, "Ali ku Nayoti ku Rama."
23 Choncho Sauli anapita ku Nayoti ku Rama. Koma Mzimu wa Mulungu
unafikanso pa iye ndipo ankalosa akuyenda mpaka anafika ku Nayoti.
24 Nayenso anavula zovala zake nayamba kulosa pamaso pa Samueli.
Kenaka anagona wamaliseche tsiku lonse ndi usiku wonse. N'chifukwa
chake anthu amati, "Kodi Sauli alinso mmodzi wa aneneri?"

# 20

*Davide ndi Yonatani*

1 Tsono Davide anathawa ku Nayoti ku Rama ndi kupita kwa Yonatani
ndipo anamufunsa kuti, "Kodi ine ndinachita chiyani? Kodi ndi-
nalakwa chiyani? Kodi abambo ako ndinawalakwira chiyani kuti azifuna
kundipha?"
2 Yonatani anayankha kuti, "Sizitheka! Iwe sufa ayi! Taona abambo anga
sachita chinthu chilichonse chachikulu kapena chaching'ono wosandi-
wuza ine. Tsopano abambo anga angandibisire bwanji zimenezi?
Sichoncho ayi."
3 Koma Davide analumbira kuti, "Abambo ako akudziwa bwino lomwe
kuti iwe umandikonda ndipo iwo amaganiza kuti, Yonatani sayenera
kudziwa zimenezi mwina adzamva chisoni kwambiri. Komabe, pali
Yehova ndi pali iwe, imfa sinanditalikire."

4 Yonatani anawuza Davide kuti, “Chilichonse chimene iwe ukufuna kuti
ndichite, ndidzakuchitira.”

5 Ndipo Davide anati, “Taona mawa ndi tsiku la chikondwerero cha
mwezi watsopano, ndipo ine ndiyenera kukadya ndi mfumu. Koma
undilole ndipite ndikabisale m’munda mpaka mkuja madzulo. 6 Ngati
abambo ako akafunsa za ine, ukawawuze kuti, ‘Davide anandiwumiriza
kuti ndimulole apite msanga kwawo ku Betelehemu, chifukwa akupereka
nsembe yapachaka ya banja lonse.’ 7 Akanena kuti, ‘Wachita bwino,’
ndiye kuti zinthu zindiyendera bwino ine mtumiki wako. Koma ngati
akapsa mtima, ndiye udziwe kuti iwo atsimikiza zondichita zoyipa.
8 Koma undikomere mtima ine mtumiki wako, pakuti unapangana nane
pangano pamaso pa Yehova. Ngati ndine wolakwa undiphe ndiwe, koma
usandipereke kwa abambo ako.”

9 Yonatani anati, “Sizitheka! Ndikanadziwa kuti abambo anga atsimikiza
kuti akuchite choyipa, kodi sindikanakuwuza?”

10 Davide anafunsa kuti, “Adzandiwuza ndani ngati abambo ako
akuyankhe mwaukali?”

11 Yonatani anawuza Davide kuti, “Tiyeni tikayende ku mundako.”
Ndipo anapita onse awiri.

12 Kenaka Yonatani anawuza Davide kuti, “Yehova Mulungu wa Israeli
akhale mboni! Ine ndikadzafunsa abambo anga nthawi yonga ino
mmawa kapena mkuja, ndipo ndikadzapeza kuti akukufunira zabwino,
ine ndidzatuma mawu kuti udziwe. 13 Koma ngati abambo anga atsimikiza
kukuchita choyipa, Yehova andilange ine Yonatani, ndipotu kwambiri
ngati sindidzakudziwitsa ndi kukulola kuti upite mu mtendere. Yehova
akhale nawe monga anakhalira ndi abambo anga. 14 Ndikakhalabe ndi
moyo udzandionetse kukoma mtima monga kwa Yehova nthawi yonse
ya moyo wanga, kuti ine ndisaphedwe. 15 Ndipo usadzaleke kuchitira
chifundo banja langa. Pamene Yehova adzawatha adani onse a Davide
pa dziko lapansi.”

16 “Dzina la ine Yonatani lisadzafafanizidwe nawo pamodzi. Yehova
alange adani onse a Davide.” 17 Kenaka Yonatani anamulumbiritsanso
Davide kuti asaleke kumukonda, pakuti ankamukonda monga ankadzikon-
dera yekha.

18 Kenaka Yonatani anawuzanso Davide kuti, “Mawa ndi tsiku la
chikondwerero cha mwezi watsopano. Zidzadziwika kuti iwe palibe
chifukwa mpando wako udzakhala wopanda munthu. 19 Mkuja adza-
kufunafuna. Tsono udzapite pamalo pamene unabisala poyamba paja
ndipo ukadikire pa mulu wa miyala uli apowo. 20 Ine ndidzaponya
mivi itatu pambali pake, ngati ndikulasa chinthu. 21 Ndipo ndidzatuma
mnyamata ndi kuti, ‘Pita ukatole miviyo!’ Ngati ndidzanena kwa iye
kuti, ‘Taona, mivi ili mbali yakuno, kayitole,’ iwe ukatuluke, pakuti
ndikulumbira, pali Yehova Wamoyo, ndiye kuti zako zili bwino, palibe
choopsa chilichonse. 22 Koma ndikadzati, ‘Taona mivi ili patsogolo pako,’
iwe udzachoke chifukwa Yehova ndiye walola kuti uchokepo. 23 Tsono
zimene tapanganazi Yehova ndiye mboni pakati pa iwe ndi ine mpaka
muyaya.”

24 Choncho Davide anakabisala m’munda ndipo nthawi ya chikondw-
erero cha mwezi watsopano itakwana mfumu Sauli anadzakhala pansi
kuti adye. 25 Iye anakhala pa malo ake a nthawi zonse pafupi ndi
khoma moyang’anana ndi Yonatani, ndipo Abineri anakhala moyandikana

ndi Sauli, koma pa malo a Davide panalibe munthu. 26 Sauli sananene
chilichonse tsiku limenelo pakuti ankaganiza kuti “Chilipo chimene
chachitika ndi Davide. Mwina mwake ngosayenera za chipembedzo.”
27 Koma pa tsiku lachiwiri la chikondwerero cha mwezi watsopano
pamalo pa Davide panalibenso munthu. Kenaka Sauli anafunsa Yonatani
kuti, “N’chifukwa chiyani mwana wa Yese sanabwere kudzadya, dzulo
ngakhale lero?”

28 Yonatani anayankha kuti, “Davide anandiwumiriza kuti ndimulole
kuti apite ku Betelehemu. 29 Anati, ‘Undilole ndipite, chifukwa banja lathu
likupereka nsembe mu mzindamo ndipo m’bale wanga wandiwumiriza
kuti ndikakhale nawo. Ngati wandikomera mtima, chonde ndilole ndipite
ndikaone abale anga.’ N’chifukwa chake sanabwere kudzadya ndi
mfumu.”

30 Sauli anamupsera mtima Yonatani ndipo namuwuza kuti, “Iwe
mwana wobadwa mwa mkazi wamakhalidwe oyipa ndi wowukira! Kodi
ukuyesa kuti ine sindikudziwa kuti umagwirizana ndi mwana wa Yese,
amene akufuna kukuchititsa manyazi iwe ndi amayi ako? 31 Mwana wa
Yese akakhala ndi moyo pa dziko lapansi lino, iwe sudzakhala mfumu.
Tsopano tumiza munthu akamutenge kubwera naye kwa ine, pakuti
Davide ayenera kufa basi!”

32 Yonatani anafunsa abambo ake kuti, “N’chifukwa chiyani mufuna kuti
Davide aphedwe? Iye walakwa chiyani?” 33 Apo Sauli anamuponyera
mkondo wake kuti amuphe. Tsono Yonatani anadziwa kuti abambo ake
atsimikiza mtima kuti aphe Davide.

34 Yonatani anachoka pa tebulopo ali wopsa mtima kwambiri. Tsiku
lachiwiri la chikondwererocho Yonatani sanadye chakudya. Iye anawaw-
idwa mtima chifukwa abambo ake anatsimikiza zakupha Davide.

35 Tsono mmawa Yonatani anapita ku munda kumene anapangana
ndi Davide. Anali ndi mnyamata wake. 36 Tsono anawuza mnya-
matayo kuti, “Thamanga ukatole muvi umene nditi ndiponye.” Mnya-
matayo akuthamanga Yonatani anaponya muvi patsogolo pa mnyamatayo.
37 Mnyamatayo atafika pamene muvi wa Yonatani unagwera, 38 Yonatani
anayitananso mnyamatayo kuti, “Fulumira, pita msanga usayime.” Chon-
cho mnyamatayo anatola muvi uja ndi kubwera nayo kwa mbuye wake.
39 (Mnyamatayo sanadziwe chimene chimachitika koma Yonatani ndi
Davide ndiwo ankadziwa). 40 Pambuyo pake Yonatani anapereka zida zake
za nkhondo kwa mnyamatayo ndipo anati, “Pita, nyamula ubwerere nazo
ku mzinda.”

41 Mnyamatayo anapita. Kenaka Davide anatuluka ku mbali ina ya
mulu wa miyala uja, nadzigwetsa pansi ndi kugunditsa nkhope yake pansi
katatu. Anapsompsona nayamba kulira onse awiri, koma Davide analira
kwambiri.

42 Yonatani anawuza Davide kuti, “Pita mu mtendere pakuti ife awiri
tinalumbira m’dzina la Yehova kuti, ‘Yehova ndiye akhale mboni pakati
pa iwe ndi ine ndiponso pakati pa zidzukulu zako ndi zidzukulu zanga kwa
nthawi yonse.’ ” Kenaka Davide anachoka, ndipo Yonatani anabwerera ku
mzinda kuja.

# 21

*Davide Apita ku Nobi*

1 Davide anapita ku Nobi kwa wansembe Ahimeleki. Ahimelekiyo
ankanjenjemera pamene ankamuchingamira, ndipo anafunsa kuti, “Muli
nokha chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani mulibe wokuperekezani?”
2 Davide anayankha Ahimeleki kuti, “Mfumu yandituma zinthu zina
ndipo yandiwuza kuti, ‘Munthu aliyense asadziwe za zimene ndakutu-
mazo.’ Kunena za anthu anga, ndawawuza kuti tikakumane pamalo pena
pake. 3 Kodi muli ndi chakudya? Patseniko malofu a buledi asanu, kapena
chilichonse muli nacho.”
4 Koma wansembeyo anamuyankha Davide kuti, “Ine ndilibe buledi
wamba woti ndikupatseni. Koma pali buledi wachipembedzo yekha. Ngati
anthu amene muli nawo sanagone ndi akazi awo mukhoza kudya.”
5 Davide anayankha kuti, “Kunena zoona sitinakhudzane ndi mkazi
monga timachitira nthawi zonse tikakhala pa ulendo. Anthu anga salola
kudziyipitsa ndi mkazi ngakhale pa ulendo wamba. Nanji lero tili
pa ulendo woterewu!” 6 Choncho wansembe uja anamupatsa buledi
wachipembedzo popeza kunalibeko buledi wina aliyense koma yekhayo
amene amaperekedwa kwa Yehova. Uyu ndi amene anachotsedwa tsiku
limenelo kuti ayikepo wina wotentha.
7 Koma tsiku limenelo mmodzi wa antchito a Sauli anali pomwepo
kudikirira kuti achite mwambo wa chipembedzo m’nyumba ya Mulungu.
Munthuyu dzina lake anali Doegi Mwedomu, munthu wamphamvu pakati
pa abusa a Sauli.
8 Davide anafunsa Ahimeleki kuti, “Kodi muli ndi mkondo kapena
lupanga pano? Ine sindinatenge lupanga langa kapena chida china
chilichonse chifukwa zimene andituma amfumu ndi zamsangamsanga.”
9 Wansembeyo anayankha kuti, “Kuno kuli lupanga la Goliati Mfilisiti
uja amene unamupha m’chigwa cha Ela, lakulungidwa m’nsalu paseli pa
Efodi. Ngati mufuna kulitenga, tengani popeza kuno kulibe lina koma
lokhalo.”
Davide anati, “Palibe lina lofanana nalo. Ndipatseni lomwelo.”

*Davide ku Gati*

10 Tsiku lomwelo Davide ananyamuka kuthawa Sauli ndipo anapita kwa
Akisi, mfumu wa ku Gati. 11 Koma nduna za Akisi zinafunsa mfumuyo
kuti, “Kodi uyu si Davide mfumu ya dzikoli? Kodi iyeyu si uja pomuvinira
ankayimba kuti,
“Sauli wapha 1,000,
koma Davide wapha miyandamiyanda?”
12 Mawu amenewa anamulowa kwambiri Davide mu mtima ndipo
anayamba kuopa kwambiri Akisi mfumu ya ku Gati. 13 Choncho anasintha
makhalidwe ake pamaso pawo, n’kudzisandutsa ngati wamisala. Iye
ankangolembalemba pa zitseko za chipata ndi kumangotuluka dovi,
n’kumayenderera m’ndevu zake.
14 Akisi anawuza nduna zake kuti, “Mukumuona munthu uyu kuti
ndi wamisala! N’chifukwa chiyani mukubwera naye kwa ine? 15 Kodi
ine ndikusowa anthu amisala kuti muzibwera naye munthuyu kwa ine
kuti azidzachita zamisala zake pamaso panga? Kodi munthu ameneyu
n’kulowa m’nyumba mwanga?”

## 22

*Davide Apita ku Adulamu ndi ku Mizipa*

1 Davide anachoka kumeneko nathawira ku phanga la Adulamu. Abale
ake ndi banja lonse la abambo ake anamva izi, anapita kumene kunali
Davide. 2 Ndipo aliyense amene anali pa mavuto, kapena ndi ngongole
kapenanso amene anali wosakondwa anasonkhana kwa iye, ndipo iye
anakhala mtsogoleri wawo. Onse pamodzi analipo amuna 400.

3 Kuchokera kumeneko Davide anapita ku Mizipa ku Mowabu ndipo
anapempha mfumu ya Mowabu kuti, “Bwanji abambo ndi amayi anga
akhale nanu mpaka ine nditadziwa chimene Mulungu adzachite nane?”
4 Choncho iye anawasiya kwa mfumu ya Mowabu ndipo anakhala naye
nthawi yonse imene Davide ankabisala ku phanga kuja.

5 Koma mneneri Gadi anawuza Davide kuti, “Usakhale ku phanga kuno.
Pita ku dziko la Yuda.” Kotero Davide anachoka ndi kupita ku nkhalango
ya Hereti.

### *Sauli Apha Ansembe a ku Nobi*

6 Tsono Sauli anamva kuti Davide ndi anthu ake apezeka. Nthawiyo
n’kuti Sauli atakhala pansi pa mtengo wa bwemba pa phiri la ku Gibeya,
mkondo uli m’dzanja lake ndi ankhondo ake atayima chomuzungulira.
7 Tsono Sauli anafunsa ankhondo ake aja kuti, “Tamverani inu anthu
a fuko la Benjamini! Kodi mwana wa Yese adzakupatsani nonsenu
minda ndi minda ya mpesa? Kodi nonsenu adzakuyikani kukhala
atsogoleri a magulu ankhondo? 8 Mwinatu n’chifukwa chake mwagwi-
rizana zondichita chiwembu. Palibe amene anandiwuza pamene mwana
wanga ankapanga pangano ndi mwana wa Yese. Palibe aliyense amene
ankalabadirako za ine kapena kundiwuza kuti mwana wanga wautsa
mtima wa wantchito wanga kuti andiwukire monga wachitira lero.”

9 Koma Doegi Mwedomu anayima pafupi ndi nduna za Sauli nati, “Ine
ndinaona mwana wa Yese atabwera kwa Ahimeleki mwana wa Ahitubi
ku Nobi. 10 Ahimelekiyo anafunsa kwa Yehova chomwe Davide ayenera
kuchita. Iye anamupatsa zakudya ndiponso lupanga la Goliati Mfilisiti
uja.”

11 Pamenepo mfumu inayitanitsa wansembe Ahimeleki mwana wa
Ahitubi ndi banja lonse la abambo ake, amene anali ansembe ku Nobi.
Ndipo onse anabwera kwa mfumu. 12 Sauli anati, “Tsono tamvera, mwana
wa Ahitubi.”

Iye anayankha kuti, “Inde mbuye wanga.”

13 Sauli anamufunsa kuti, “N’chifukwa chiyani iwe ndi mwana wa Yese
mwandiwukira ine? Wamupatsa buledi ndi lupanga. Wafunsiranso kwa
Yehova zoti andiwukire ndi kundibisalira monga wachita leromu?”

14 Ahimeleki anayankha mfumu kuti, “Kodi ndani mwa ankhondo anu
onse amene ali wokhulupirika monga Davide? Iye uja ndi mkamwini
wa mfumu, kapitawo wa asilikali okutetezani ndiponso munthu amene
amalemekezedwa m’banja lanu? 15 Kodi tsiku limeneli linali loyamba kuti
ndimufunsire kwa Yehova? Ayi sichoncho! Mfumu musandinenere kan-
thu kalikonse koyipa kapena banja la abambo anga, pakuti sindikudziwa
kanthu kena kalikonse ka zimenezi.”

16 Koma mfumu inati, “Iwe Ahimeleki ndi banja lonse la abambo ako
mudzaphedwa ndithu.”

17 Kenaka mfumu inalamulira alonda amene anali naye kuti, “Iphani
ansembe a Yehovawa chifukwa iwo akugwirizana ndi Davide. Iwo
amadziwa kuti Davide ankathawa koma sanandiwuze.”

Koma antchito a mfumu aja sanasamule dzanja kuti aphe ansembe a
Yehova.
18 Kotero mfumu inalamula Doegi kuti, “Uwaphe ndiwe ansembewa.”
Choncho Doegi Mwedomu anapita ndi kuwapha. Tsiku limenelo iye
anapha amuna 85 amene amavala efodi wa nsalu yofewa. 19 Kunena
za Nobi, mzinda wa ansembe, Sauli anapha amuna ndi amayi, ana ndi
makanda pamodzi ndi ng’ombe, abulu ndi nkhosa.

20 Koma Abiatara mwana wa Ahimeleki mwana wa Ahitubi anapulu-
muka ndi kuthawira kwa Davide. 21 Abiatara anawuza Davide kuti Sauli
wapha ansembe a Yehova. 22 Ndipo Davide anati kwa Abiatara, “Tsiku
lija pamene Doegi Mwedomu anali kumene kuja, ine ndimadziwa kuti
salephera kukamuwuza Sauli. Ine ndi amene ndaphetsa banja lonse la
abambo ako. 23 Iwe khala ndi ine, usaope munthu amene akufuna moyo
wako komanso wanga. Udzatetezeka ukakhala ndi ine.”

# 23

### *Davide Apulumutsa Mzinda wa Keila*

1 Davide atawuzidwa kuti “Onani, Afilisti akuthira nkhondo mzinda wa
Keila ndi kulanda zokolola zawo za m’nkhokwe,” 2 anafunsa Yehova kuti,
“Kodi ndipite ndikamenyane nawo Afilistiwa?”

Yehova anamuyankha kuti, “Pita, kamenyane nawo Afilisti ndi kupulu-
mutsa mzinda wa Keila.”

3 Koma anthu amene anali ndi Davide anati, “Ngati tikuchita mantha
ku Yuda konkuno, nanji kupita ku Keila kukamenyana ndi ankhondo a
Afilisti!”

4 Davide anafunsanso Yehova, ndipo Yehova anamuyankha kuti, “Pita
ku Keila pakuti ndapereka Afilisti m’dzanja lako.” 5 Choncho Davide ndi
anthu ake anapita ku Keila kukamenyana ndi Afilisti. Anapha Afilisti
ambiri ndi kutenga ziweto zawo. Choncho anapulumutsa anthu a ku
Keila. 6 (Pamene Abiatara mwana wa Ahimeleki anathawira kwa Davide
anabwera ndi efodi m’manja mwake).

### *Sauli Atsatira Davide*

7 Sauli atamva kuti Davide wapita ku Keila anati, “Mulungu wamu-
pereka kwa ine, pakuti Davide wadzitsekera yekha m’ndende polowa
mu mzinda umene uli ndi zipata ndi zotsekera zake.” 8 Choncho Sauli
anasonkhanitsa ankhondo ake nawatuma ku Keila kuti akamuzungulire
Davide ndi anthu ake.

9 Davide atadziwa kuti Sauli akufuna kumuchita chiwembu, anawuza
Abiatara wansembe uja kuti, “Bwera nayo efodiyo.” 10 Tsono Davide
anayankhula ndi Yehova kuti, “Inu Yehova Mulungu wa Israeli, ine
mtumiki wanu ndamva ndithu kuti Sauli akufuna kubwera ku Keila
ndi kudzawononga mzindawu chifukwa cha ine. 11 Kodi anthu a
Keila adzandipereka m’manja mwa Sauli? Kodi Sauli abweradi monga
ndamvera ine mtumiki wanu? Inu Yehova Mulungu wa Israeli, chonde,
ndiwuzeni ine mtumiki wanu.”

Ndipo Yehova anati, “Sauli abweradi.”

12 Davide anafunsanso, “Kodi anthu a ku Keila adzapereka ine ndi anthu
angawa kwa Sauli?”

Ndipo Yehova anayankha, “Iwo adzakuperekanidi.”

13 Choncho Davide ndi anthu ake, omwe analipo 600, anachoka ku Keila
namayenda mothawathawa. Sauli atamva kuti Davide wathawa ku Keila,
sanatumizeko ankhondo ake aja.
14 Davide ankakhala m'mapanga m'dziko lamapiri ku chipululu cha Zifi.
Sauli ankamufufuza tsiku ndi tsiku, koma Mulungu sanapereke Davide
m'manja mwake.
15 Davide anaona kuti Sauli akufunafuna kuti amuphe. Nthawiyi n'kuti
Davide ali m'chipululu cha Zifi ku Horesi. 16 Ndipo Yonatani mwana
wa Sauli anapita kwa Davide ku Horesi ndipo anamulimbitsa mtima
pomuwuza kuti Yehova ali naye. 17 Iye anamuwuza kuti, "Usaope,
abambo anga sadzakupha. Iwe udzakhala mfumu ya Israeli ndipo ine
ndidzakhala wachiwiri wako. Ngakhale abambo anga Sauli akudziwa
zimenezi." 18 Awiriwa anachita pangano pamaso pa Yehova. Ndipo
Yonatani anabwerera kwawo, koma Davide anakhalabe ku Horesi.
19 Anthu a ku Zifi anapita kwa Sauli ku Gibeya ndipo anamuwuza kuti,
"Davide akubisala kwathu, m'mapanga a ku Horesi, m'phiri la Hakila,
kummwera kwa Yesimoni. 20 Tsopano inu, mubwere nthawi iliyonse
imene mukufuna, ndipo ife tidzamupereka kwa mfumu."
21 Sauli anayankha kuti, "Yehova akudalitseni pakuti mwandichitira
chifundo. 22 Pitani mukatsimikizire. Mukaone kumene amakhala
ndiponso mupeze munthu amene wamuona. Anthu amandiwuza kuti
ndi wochenjera kwambiri. 23 Kafufuzeni ndithu malo onse kumene am-
abisalako, ndipo mubwerenso kuno mudzandiwuze chenicheni. Pambuyo
pake ine ndidzapita nanu. Ngatidi ali m'deralo ndidzamusaka pakati pa
mabanja onse a Yuda."
24 Kotero iwo ananyamuka ndi kupita ku Zifi, koma Sauli asananyamuke.
Nthawi imeneyi Davide ndi anthu ake anali ku chipululu cha Maoni,
ku Araba kummwera kwa Yesimoni. 25 Sauli ndi anthu ake anapita
kukamufufuza Davide. Koma Davide atamva izi anathawa ndi kukabisala
ku thanthwe la chipululu cha Maoni. Sauli atamva kuti Davide anathawira
ku Maoni anamutsatira ku chipululu komweko.
26 Sauli amayenda mbali ina ya phirilo, ndipo Davide ndi anthu ake
nawonso anali mbali ina ya phirilo. Koma Davide ndi anthu ake
anafulumira kumuthawa Sauli pamene Sauliyo ndi anthu ake ali pafupi
kuwagwira. 27 Nthawi yomweyo munthu wina wamthenga anabwera
kudzamuwuza Sauli kuti, "Bwerani msanga! Afilisti akuthira nkhondo
dzikoli." 28 Choncho Sauli analeka kuthamangitsa Davide ndipo anapita
kukamenyana ndi Afilisti. N'chifukwa chake malowa amatchedwa Mwala
wa Malekano. 29 Ndipo Davide anachoka kumeneko ndi kukakhala ku
mapanga a ku Eni Gedi.

# 24

*Davide Amusiya Sauli Wosamupha*

1 Sauli atabwera kuchokera kumene amathamangitsa Afilisti anamva
kuti, "Davide ali m'chipululu cha Eni Gedi." 2 Tsono Sauli anatenga
asilikali 3,000 odziwa kumenya bwino nkhondo kuchokera pakati pa
Aisraeli onse ndipo anapita kukafunafuna Davide ndi anthu ake ku
Matanthwe a Mbalale.
3 Iye anafika ku makola a nkhosa amene anali m'mbali mwa njira.
Kumeneko kunali phanga, ndipo Sauli analowa m'phangamo kuti
akadzithandize. Davide ndi anthu ake ankabisala m'kati mwenimweni

mwa phangalo. 4 Tsono anthu a Davide anamuwuza kuti, “Tsiku lija
lafika limene Yehova anakuwuzani kuti, ‘Ndidzapereka mdani wanu
m’manja mwanu, ndi kumuchita chimene chidzakukomereni.’ ” Koma
Davide anapita mwakachetechete ndi kukadula msonga ya mkanjo wa
Sauli.
5 Atachita izi, Davide anatsutsika mu mtima chifukwa anadula msonga
ya mkanjo wa Sauli. 6 Tsono anawuza anthu ake kuti, “Yehova asalole kuti
ndimuchite choyipa mbuye wanga, wodzozedwa wa Yehova. Ndisamup-
weteke pakuti ndi wodzozedwa wa Yehova.” 7 Choncho Davide anabweza
mitima ya anthu ake ndi mawu amenewa, ndipo sanawalole kuti aphe
Sauli. Pambuyo pake Sauli anatuluka m’phangamo ndipo anachoka.
8 Kenaka Davide anatuluka m’phanga muja ndipo anayitana Sauli,
“Mbuye wanga!” Sauli atayang’ana m’mbuyo, Davide anawerama ndi
kugunditsa nkhope yake pansi. 9 Anafunsa Sauli kuti, “N’chifukwa
chiyani mumamvera mawu a anthu kuti, ‘Davide wakukonzerani chi-
wembu?’ 10 Lero lino inu mwadzionera nokha kuti Yehova anakuperekani
m’manja mwanga m’phanga muja. Ena anandiwuza kuti ndikupheni,
koma ndakusiyani. Ndinati, ‘Sindidzapha mbuye wanga pakuti ndiye
wodzozedwa wa Yehova.’ 11 Tsono abambo anga, onanitu kansalu ka
mkanjo wanu kali m’dzanja langali! Popeza kuti ndinatha kudula msonga
ya mkanjo wanu koma osakuphani, pamenepo mudziwe kuti ine ndilibe
maganizo woti ndikuchiteni choyipa kapena kukuwukirani. Sindinaku-
lakwireni ngakhale kuti inu mukufuna moyo wanga kuti mundiphe.
12 Yehova aweruze pakati pa inu ndi ine, akulangeni chifukwa cha zoyipa
zimene mukundichitazi, koma dzanja langa silidzakukhudzani. 13 Paja
anthu akale anati, ‘Munthu woyipa, ntchito zakenso ndi zoyipa.’ Kotero
dzanja langa silidzakukhudzani.
14 “Kodi mfumu ya Israeli yadzalondola yani. Inu mukuthamangitsa
yani? Galu wakufa kodi? Nsabwe kodi? 15 N’chifukwa chake Yehova
agamule, inde aweruze pakati pa inu ndi ine ndi kupeza wolakwa. Yehova
anditeteze ndi kundipulumutsa m’dzanja lanu.”
16 Davide atatsiriza kuyankhula mawu awa, Sauli anafunsa kuti, “Kodi
mawu amenewa ndi akodi mwana wanga Davide?” Sauli anayamba kulira
mokweza. 17 Anawuza Davide kuti, “Ndiwe wolungama kuposa ine. Iwe
wandikomera mtima pamene ine ndakuchitira zoyipa. 18 Iweyo lero lino
wandifotokozera zabwino zimene wandichitira. Yehova anandipereka
m’dzanja lako koma iwe sunandiphe. 19 Kodi munthu atapeza mdani
wake angamulole kuti apite wosamuvulaza? Motero Yehova akuchitire
iwe zabwino chifukwa cha zimene wandichitira lerozi. 20 Ona tsono,
Ine ndikudziwa kuti udzakhala mfumu ndithu ndipo ufumu wa Israeli
udzakhazikika m’manja mwako. 21 Tsopano undilonjeze molumbira lero
m’dzina la Yehova kuti sudzapha zidzukulu zanga ine nditamwalira
kapena kufuta dzina langa pa banja la makolo anga.”
22 Choncho Davide analumbira pamaso pa Sauli. Pambuyo pake Sauli
anabwerera kwawo, koma Davide ndi anthu ake anapitanso ku phanga
kuja.

# 25

*Davide, Nabala ndi Abigayeli*

1 Samueli anamwalira, ndipo Aisraeli onse anasonkhana kudzalira
maliro ake ndipo anamuyika m’manda ku mudzi kwawo ku Rama.

Ndipo Davide anapita ku chipululu cha Parani. [2] Kunali munthu wina
wolemera kwambiri ku Maoni amene malo ake a ntchito anali ku Karimeli.
Iyeyu anali ndi mbuzi 1,000 ndi nkhosa 3,000. [3] Dzina lake linali Nabala
ndipo anali wa fuko la Kalebe. Dzina la mkazi wake linali Abigayeli.
Anali mkazi wanzeru ndi wokongola, koma mwamuna wake, wa banja
la Kalebe, anali wowuma mtima ndi wamwano pa zochita zake.

[4] Davide anamva akanali ku chipululu kuti Nabala akumeta nkhosa.
[5] Choncho anatuma anyamata khumi nawawuza kuti, "Pitani kwa Nabala
ku Karimeli ndipo mukamulonjere m'dzina langa. [6] Mukamuwuze kuti,
'Mtendere ukhale ndi inu, banja lanu pamodzi ndi zonse zimene muli
nazo.

[7] " 'Tsono ndamva kuti muli ndi anthu ometa nkhosa. Pamene abusa anu
anali nafe kuno, sitinawachite china chilichonse choyipa, ndipo sanasowe
kanthu pa nthawi yonse imene anali ku Karimeli. [8] Muwafunse antchito
anu ndipo akuwuzani. Kotero akomereni mtima anyamata anga, pakuti
tabwera pa nthawi yachikondwerero. Chonde apatseniko antchito anuwo
ndi mwana wanu Davide chilichonse chimene mungakhale nacho.' "

[9] Anyamata a Davide aja atafika, anamuwuza Nabala zonse zimene
Davide anayankhula. Ndipo anadikira yankho.

[10] Nabala anayankha anyamata a Davide kuti, "Kodi Davide ndi ndani?
Mwana wa Yese ndi ndani? Masiku ano pali antchito ambiri amene
akuthawa kwa mabwana awo. [11] Nditengerenji buledi, madzi ndi nyama
zimene ndaphera anthu anga ometa nkhosa ndi kuzipereka kwa anthu
amene sindikudziwa kumene achokera?"

[12] Choncho anyamata a Davide aja anatembenuka nabwerera. Atafika
anafotokozera Davide mawu onse a Nabala. [13] Davide anawuza anthu ake
kuti, "Aliyense amangirire lupanga lake!" Choncho aliyense anamangirira
lupanga lake. Davidenso anamangirira lupanga lake. Anthu pafupifupi
400 ndiwo anapita ndi Davide, pamene anthu 200 anatsala ndi katundu.

[14] Tsono mmodzi mwa antchito anawuza Abigayeli mkazi wa Nabala
kuti, "Davide anatumiza amithenga kuchokera ku chipululu kudzalonjera
mbuye wathu, koma iye anawalalatira. [15] Komatu anthuwa anatichitira
zabwino kwambiri. Sanatizunze, ndipo nthawi yonse imene tinali nawo
ku busa sitinasowe kanthu. [16] Ankatitchinjiriza ngati mpanda usiku
ndi usana nthawi yonse tinkaweta nkhosa. [17] Tsono onani chimene
mungachite, chifukwa zimenezi zingadzetse tsoka pa mbuye wathu
pamodzi ndi nyumba yake. Paja mbuye athu aja ndi munthu wa khalidwe
loyipa moti palibe amene angathe kuyankhula naye."

[18] Ndipo Abigayeli sanataye nthawi. Iye anatenga malofu a buledi
200, matumba a chikopa awiri a vinyo, nkhosa zisanu zowotcheratu,
makilogalamu 17 a tirigu wokazinga, makeke a mphesa zowuma 100,
ndiponso makeke a nkhuyu 200, ndipo anazisenzetsa abulu. [19] Kenaka
anawuza antchito ake kuti, "Tsogolani, ine ndikutsatirani." Koma
sanawuze mwamuna wake Nabala.

[20] Mayi uja atakwera pa bulu wake ndi kufika pa tsinde la phiri,
anangoona Davide ndi ankhondo ake akubwera kunali iye. Choncho
anakumana nawo. [21] Nthawiyi n'kuti Davide atanena kuti, "Kani
ndinalondera pachabe katundu wa munthu uyu m'chipululu muja!
Ndipotu palibe kanthu n'kamodzi komwe kake kamene kanasowa. Tsono
wandibwezera zoyipa m'malo mwa zabwino. [22] Mulungu andilange
kwambiri ngati pofika mmawa nditakhale nditasiyako ngakhale munthu
mmodzi mwa onse amene ali nawo."

23 Abigayeli ataona Davide, anatsika pa bulu wake mofulumira ndipo
anadzigwetsa pansi pamaso pa Davide. 24 Ali chigonere choncho pa
mapazi a Davide anati, "Mbuye wanga, kulakwa kukhale pa ine ndekha.
Chonde lolani kuti mdzakazi wanune ndiyankhule nanu, ndipo mumve
mawu a ine mdzakazi wanu. 25 Mbuye wanga musasamale za mwamuna
wanga Nabala, munthu wa khalidwe loyipa. Iyeyu ali monga dzina lake
liliri. Monga dzina lake litanthauza kuti chitsiru, ndiye kuti zake zonse
ndi zauchitsiru basi. Koma ine mdzakazi wanu, sindinawaone anthu
amene mbuye wanga munawatuma. 26 Tsono mbuye wanga muli apa,
ndikulumbira pali Yehova wamoyo amene wakuletsani kuti musakhetse
magazi a munthu ndi kulipsira nokha, kuti adani anu amene afuna
kukuchitani zoyipa adzakhale ngati Nabala. 27 Choncho, nazi mphatso
zimene mdzakazi wanu ndabwera nazo kwa mbuye wanga kuti zipatsidwe
kwa anyamata amene muli nawo. 28 Chonde khululukani zolakwa za ine
mdzakazi wanu. Ndithu Yehova adzakhazikitsa banja la mbuye wanga
mu ufumu, popeza mukumenya nkhondo ya Yehova. Choncho choyipa
sichidzapezeka mwa inu masiku onse a moyo wanu. 29 Ngati munthu wina
akuwukirani ndi kukulondani, Yehova Mulungu wanu adzateteza moyo
wa mbuye wanga monga mmene munthu asungira chuma m'phukusi,
koma moyo wa adani anu adzawutaya kutali monga momwe munthu
amaponyera mwala ndi legeni. 30 Yehova adzakuchitirani mbuye wanga
zabwino zonse zimene anakulonjezani. Adzakuyikani kukhala wolamulira
Aisraeli. 31 Zikadzatero, inu mbuye wanga simudzakhala ndi chikum-
bumtima choti munakhetsa magazi kapena kulipsira popanda chifukwa.
Koma Yehova akadzakuchitirani zabwino zonsezi musadzandiyiwale ine
mdzakazi wanu."

32 Tsono Davide anawuza Abigayeli kuti, "Alemekezeke Yehova Mulungu
wa Israeli, amene wakutuma iwe lero kuti ukumane nane. 33 Yehova
akudalitseni chifukwa cha nzeru zanu pondiletsa lero kuti ndisakhetse
magazi ndi kubwezera adani anga ndi manja anga. 34 Kunena zoona,
pali Yehova Wamoyo, Mulungu wa Israeli, amene wandiletsa kuti
ndisakupwetekeni, mukanapanda kubwera msanga kudzakumana nane,
palibe munthu aliyense wamwamuna wa Nabala akanasiyidwa wamoyo
pakucha mmawa."

35 Ndipo Davide analandira kwa mayiyo zimene anamutengera ndipo
anati, "Pitani kwanu mu mtendere. Ine ndamva mawu anu ndipo
ndavomera zimene mwapempha."

36 Abigayeli atabwerera kwa Nabala anamupeza ali m'nyumba akuchita
mphwando ngati la mfumu. Iye anali atakondwa kwambiri popeza anali
ataledzera kwambiri. Choncho mkazi wakeyo sanamuwuze kalikonse
mpaka mmawa kutacha. 37 Tsono mmawa, mowa utamuchoka Nabala,
mkazi wake anamuwuza zonse. Pomwepo mtima wake unaleka kugunda
ndipo unawuma gwaa ngati mwala. 38 Patapita masiku khumi, Yehova
anakantha Nabala ndipo anafa.

39 Pamene Davide anamva kuti Nabala wamwalira, iye anati, "Ale-
mekezeke Yehova, walipsira Nabala chipongwe chimene anandichita
ndipo anandiletsa ine mtumiki wake kuti ndisachite choyipa. Yehova
wabwezera pamutu pa Nabala choyipa chimene iye anachita."

Kenaka Davide anatumiza mawu kwa Abigayeli, kumupempha kuti
akhale mkazi wake. 40 Anyamata a Davide atafika ku Karimeli anawuza
Abigayeli kuti, "Davide watituma kwa iwe kuti tikutenge ukhale mkazi
wake."

41 Abigayeli anagwada nagunditsa nkhope yake pansi ndipo anati, “Ine
mdzakazi wa mbuye wanga ndakonzeka kutumikira ngakhale kusambitsa
mapazi a anyamata ake.” 42 Motero Abigayeli ananyamuka mofulumira
nakwera bulu wake. Tsono iye pamodzi ndi anamwali ake asanu
amene ankamutumikira, anatsagana ndi amithenga a Davide aja ndipo
anakakhala mkazi wake wa Davide. 43 Davide n’kuti atakwatiranso
Ahinoamu wa ku Yezireeli ndipo onse awiri anali akazi ake. 44 Koma Sauli
anali atakwatitsa Mikala, mkazi wa Davide kwa Paliti mwana wa Laisi wa
ku Galimu.

# 26

*Davide Apewa Kupha Sauli Kachiwiri*

1 Anthu a ku Zifi anapita kwa Sauli ku Gibeya nati, “Davide akubisala
ku phiri la Hakila, limene limayang’anana ndi Yesimoni.”

2 Choncho Sauli ananyamuka pamodzi ndi ankhondo ake 3,000 napita ku
chipululu cha Zifi kukafunafuna Davide ku chipululuko. 3 Sauli anamanga
msasa wake m’mbali mwa njira yopita ku phiri la Hakila moyang’anana
ndi Yesimoni. Koma Davide anali m’chipululumo. Davide ataona kuti
Sauli amamulondola mpaka kumeneko, 4 iye anatumiza anthu okazonda
ndipo anapeza kuti Sauli wafikadi ndithu.

5 Tsono Davide ananyamuka napita kumalo kumene Sauli anamanga
misasa. Iye anaona pamene Sauli ndi Abineri mwana wa Neri mkulu
wa ankhondo anagona. Sauli anagona m’kati mwa tenti ndipo asilikali
anagona momuzungulira.

6 Ndipo Davide anafunsa Ahimeleki Mhiti ndi Abisai mwana wa Zeruya,
m’bale wa Yowabu kuti, “Ndani adzapita nane ku msasa kwa Sauli?”

Abisai anayankha kuti, “Ine ndidzapita nanu.”

7 Choncho Davide ndi Abisai anapita ku misasa ya ankhondowo
usiku. Atafika anangopeza Sauli ali gone mu msasa wake mkondo wake
atawuzika pansi pafupi ndi mutu wake, Abineri ndi ankhondo onse anali
atagona momuzungulira.

8 Abisai anawuza Davide kuti, “Lero Mulungu wapereka mdani wanu
m’manja mwanu. Tsopano ndiloleni ndimukhomere pansi ndi mkondo
wangawu kamodzin’kamodzi. Sindimulasa kawiri.”

9 Koma Davide anamuyankha Abisai kuti, “Usamuphe! Ndani adzapha
wodzozedwa wa Yehova ndi kupezeka wosalakwa? 10 Davide anati, Pali
Yehova wamoyo, Yehova mwini ndiye adzamukanthe, mwina tsiku lake
lomwalira lidzafika, kapena adzapita ku nkhondo nakaphedwa komweko.
11 Koma Yehova andiletse kuti ndisapweteke wodzozedwa wa Yehova.
Tsopano tingotenga mkondo umene uli ku mutu kwakewo ndi botolo la
madzilo ndipo tizipita.”

12 Motero Davide anatenga mkondo ndi botolo lamadzi zimene zinali ku
mutu kwa Sauli ndipo anachoka. Palibe amene anaona zimenezi kapena
kudziwa, ndipo palibenso amene anadzuka. Onse anali m’tulo, chifukwa
Yehova anawagonetsa tulo tofa nato.

13 Pambuyo pake Davide anadutsa nakakwerera mbali ina ya phiri,
ndi kuyimirira pamwamba pa phiri patali. Pakati pawo panali mpata
waukulu. 14 Davide anayitana gulu lankhondo ndi Abineri mwana wa
Neri nawafunsa kuti, “Kodi sundiyankha ine Abineri?”

Abineri anayankha kuti, “Ndiwe yani amene ukuyitana mfumu?”

15 Davide anamufunsa Abineri kuti, “Kodi sindiwe mwamuna? Ndipo
wofanana nawe ndani mu Israeli? N’chifukwa chiyani sunateteze mbuye
wako mfumu? Munthu wina anabwera kumeneko. 16 Chimene wachita
iwe si chabwino. Pali Yehova wamoyo iwe ndi asilikali ako muyenera
kufa chifukwa simunateteze mbuye wanu, wodzozedwa wa Yehova.
Tayang’anayang’ana. Uli kuti mkondo wa mfumu ndi botolo lamadzi
zimene zinali kumutu kwa mfumu?”
17 Sauli anazindikira mawu a Davide ndipo anafunsa kuti, “Kodi
amenewa ndi mawu ako Davide mwana wanga?”
Davide anayankha, “Inde ndi anga, mbuye wanga mfumu. 18 N’chifukwa
chiyani mbuye wanga mukundilonda ine mtumiki wanu? Kodi ine
ndachita chiyani ndipo ndapezeka ndi cholakwa chotani? 19 Tsopano
mbuye wanga mfumu tamverani mawu a mtumiki wanu. Ngati ndi
Yehova wautsa mtima wanu kuti mundiwukire, ndiye alandire chipepeso.
Koma ngati ndi anthu amene achita zimene, ndiye Yehova awatemberere
popeza andipirikitsa lero kundichotsa m’dziko la Yehova, namati, ‘Pita
kapembedze milungu ina.’ 20 Tsopano musalole kuti magazi anga
akhetsedwe kutali ndi Yehova pakuti mfumu ya Israeli yatuluka kudzafu-
nafuna ine nsabwe, monga mmene munthu asakira nkhwali ku mapiri.”
21 Ndipo Sauli anati, “Ine ndachimwa. Bwerera mwana wanga
Davide. Sindidzakuchitanso choyipa popeza lero wauwona moyo wanga
ngati wamtengowapatali. Taona, ndachita zauchitsiru ndipo ndachimwa
kwambiri.”
22 Davide anayankha kuti, “Nawu mkondo wanu, mfumu. Tumani
mmodzi wa anyamata anu abwere adzatenge. 23 Yehova amadalitsa
munthu aliyense wolungama ndi wokhulupirika. Yehova anakuperekani
lero m’manja mwanga, koma ine sindinakhudze wodzozedwa wa Yehova.
24 Monga momwe ine lero ndachitira kuwuyesa moyo wanu ngati
wamtengowapatali, momwemonso Yehova awuyese moyo wanga wamten-
gowapatali ndipo andipulumutse m’mavuto anga onse.”
25 Ndipo Sauli anawuza Davide kuti, “Yehova akudalitse iwe Davide
mwana wanga. Udzachita zinthu zazikulu ndipo udzapambana.”
Choncho Davide anayenda njira yake ndipo Sauli anabwerera kwawo.

# 27

*Davide Pakati pa Afilisti*

1 Davide anaganiza mu mtima mwake nati, “Tsiku lina ine ndidza-
phedwa ndi Sauli. Palibe chabwino ndingachite, koma kuthawira ku dziko
la Afilisti. Kotero Sauli adzasiya kundifunafuna m’dziko lonse la Israeli,
ndipo ndidzapulumuka.”
2 Choncho Davide ndi anthu 600 amene anali nawo anachoka napita kwa
Akisi mwana wa Maoki mfumu ya ku Gati. 3 Davide anakhala ndi Akisi ku
Gati pamodzi ndi ankhondo ake, aliyense ndi banja lake. Davide ali ndi
akazi ake awiri, Ahinoamu wa ku Yezireeli ndi Abigayeli wa ku Karimeli,
mkazi wamasiye wa Nabala. 4 Sauli anamva kuti Davide wathawira ku
Gati, ndipo sanamufunefunenso.
5 Kenaka Davide anawuza Akisi kuti, “Ngati ndapeza kuyanja pamaso
panu mundipatse malo dera limodzi la dziko lanu kuti ndizikhala
kumeneko. Mtumiki wanu adzakhala mu mzinda waufumu chifukwa
chiyani?”

6 Choncho tsiku limenelo Akisi anamupatsa Zikilagi ndipo mzindawo
wakhala wa mafumu a Yuda mpaka lero. 7 Davide anakhala m'dziko la
Afilisti kwa chaka chimodzi ndi miyezi inayi.

8 Tsono Davide ndi anthu ake ankapita kukathira nkhondo Agesuri,
Agirizi ndi Aamaleki. (Mitundu ya anthu imeneyi kuyambira kale
inkakhala m'dziko la pakati pa Suri ndi Igupto). 9 Davide ankati akathira
nkhondo dera lina, sankasiya munthu wamoyo, mwamuna kapena mkazi,
koma ankatenga nkhosa, ng'ombe, abulu, ngamira ndi zovala, pambuyo
pake n'kubwerera kwa Akisi.

10 Akisi akafunsa kuti, "Kodi lero unapita kukathira nkhondo kuti?"
Davide ankayankha kuti, "Ndinapita kukathira nkhondo kummwera kwa
Yuda," mwinanso ankanena kuti, "Ndinapita ku dziko la Ayerahimeeli"
kapenanso ankanena kuti, "Ndinapita ku dziko la Akeni." 11 Davide
sankasiya mwamuna kapena mkazi wamoyo kuti akafotokozere anthu
a ku Gati zochitikazo kuopa kuti opulumukawo akhoza kudzanena kuti
"Davide watichita zakutizakuti." Tsono izi ndi zimene Davide ankachita
pamene ankakhala m'dziko la Afilisti. 12 Akisi ankamukhulupirira Davide
ndipo ankati mu mtima mwake, "Davide wadzisandutsa munthu woyipa
kwambiri pakati pa anthu ake omwe, Aisraeli. Tsono adzakhala mtumiki
wanga mpaka kalekale."

# 28

### *Sauli ndi Mfiti ya ku Endori*

1 M'masiku amenewo Afilisti anasonkhanitsa ankhondo awo kuti akamenyane ndi Aisraeli. Akisi anawuza Davide kuti, "Udziwe kuti iwe pamodzi ndi anthu ako mudzapita nane ku nkhondo."

2 Davide anayankha kuti, "Tsono inu mudzaona zimene mtumiki wanune ndingachite."

Akisi anayankha kuti, "Chabwino ine ndidzakuyika iwe kukhala mlonda wanga moyo wako wonse."

3 Nthawi imeneyi n'kuti Samueli atamwalira, ndipo Aisraeli onse anamulira namuyika m'manda ku mzinda wake wa Rama. Sauli anali atachotsa m'dzikomo anthu owombeza mawula ndi woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa.

4 Tsono Afilisti anasonkhana nabwera kudzamanga misasa yawo ku
Sunemu. Nayenso Sauli anasonkhanitsa Aisraeli onse ndi kumanga misasa
yawo ku Gilibowa. 5 Sauli ataona gulu lankhondo la Afilisti anaopa ndipo
ananjenjemera kwambiri. 6 Choncho Sauli anafunsa nzeru kwa Yehova
koma Yehova sanamuyankhe ngakhale kudzera m'maloto, kapena mwa
Urimu ngakhalenso kudzera mwa aneneri. 7 Kenaka Sauli anawuza nduna
zake kuti, "Mundipezere mkazi amene amawombeza mawula kuti ndipite
ndikafunse kwa iye."

Nduna zakezo zinamuyankha kuti, "Alipo mkazi woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa ku Endori."

8 Kotero Sauli anadzizimbayitsa navala zovala zachilendo. Tsono iye pamodzi ndi anthu awiri anapita nakafika kwa mkazi uja usiku, ndipo anamupempha kuti, "Chonde ndifunsireni nzeru kwa mizimu ya anthu akufa. Koma makamaka munditulutsire mzimu wa amene ndimutchule."

9 Koma mkaziyo anayankha kuti, "Ndithu inu mukudziwa chimene Sauli anachita. Paja iye anachotsa m'dziko muno anthu onse owombeza ndi

woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa. Chifukwa chiyani mukutchera moyo wanga msampha kuti ndiphedwe?”

10 Koma Sauli analonjeza mkaziyo molumbira nati, “Pali Yehova wamoyo, iweyo sudzalangidwa chifukwa cha zimenezi.”

11 Kenaka mkaziyo anafunsa, “Ndikuyitanireni yani?”

Iye anati, “Undiyitanire Samueli.”

12 Pamene mkaziyo anaona Samueli anakuwa kwambiri, nawuza Sauli kuti, “N’chifukwa chiyani inu mwandipusitsa? Inu ndinu Sauli!”

13 Mfumuyo inamuwuza kuti, “Usaope. Kodi ukuona chiyani?”

Mkaziyo anayankha kuti, “Ndikuona mzimu ukutuluka pansi.”

14 Sauli anafunsa, “Kodi mzimuwo ukuoneka motani?”

Mkaziyo anayankha kuti, “Amene akutuluka ndi munthu wokalamba ndipo wavala mkanjo.”

Apo Sauli anadziwa kuti anali Samueli ndipo anawerama nagunditsa nkhope yake pansi.

15 Samueli anafunsa Sauli kuti, “N’chifukwa chiyani wandivutitsa pondiyitana kuti ndibwere kuno?”

Sauli anayankha kuti, “Ine ndavutika kwambiri m’maloto. Afilisti akumenyana nane, ndipo Mulungu wandifulatira. Iye sakundiyankhulanso, ngakhale kudzera mwa aneneri kapena maloto. Choncho ndakuyitanani kuti mundiwuze zoti ndichite.”

16 Samueli anati, “N’chifukwa chiyani ukundifunsa ine, pakuti tsopano
Yehova wakufulatira ndipo wasanduka mdani wako? 17 Yehova wakuchita
zimene ananeneratu kudzera mwa ine. Yehova wachotsa ufumu m’manja
mwako ndipo waupereka kwa mnansi wako, kwa Davide. 18 Yehova
wachita zimenezi lero chifukwa sunamvere mawu ake ndipo sunawa-
wonongeretu Aamaleki. 19 Yehova adzapereka ndithu iweyo pamodzi ndi
Aisraeli kwa Afilisti. Ndipo mmawa iweyo ndi ana ako mudzakhala ndi ine
kuno. Ndithu Yehova adzapereka gulu lankhondo la Aisraeli kwa Afilisti.”

20 Nthawi yomweyo Sauli anagwa pansi atadzazidwa ndi mantha chifukwa cha mawu a Samueli. Analibenso mphamvu, pakuti sanadye tsiku lonse.

21 Mkazi uja tsono anasendera kufupi ndi Sauli, ndipo ataona kuti
Sauli akuchita mantha, anamuwuza kuti, “Taonani, mdzakazi wanune
ndakumverani. Ndayika moyo wanga pa chiswe ndipo ndamvera
zimene munandiwuza. 22 Tsono inunso mumvere mawu a mdzakazi
wanune. Mundilole kuti ndikupatseni ka buledi pang’ono kuti mukhale
ndi mphamvu zoyendera pa ulendo wanu.”

23 Iye anakana ndipo anati, “Ayi, ine sindidya.”

Koma nduna zake pamodzi ndi mkaziyo anamuwumiriza, ndipo anawamvera. Choncho anadzuka pansi nakhala pa bedi.

24 Mkaziyo anali ndi mwana wang’ombe wonenepa ndipo anamupha
mwachangu. Anatenga ufa nawukanyanga ndipo anaphika buledi
wopanda yisiti. 25 Tsono anapereka bulediyo kwa Sauli ndi nduna
zake ndipo anadya. Pambuyo pake ananyamuka kupita kwawo usiku
womwewo.

# 29

*Afilisti Akana Davide*

1 Afilisti anasonkhanitsa asilikali awo onse ku Afeki, ndipo Israeli
anamanga misasa yawo pa chitsime cha Yezireeli. 2 Pamene atsogoleri a

Afilisti ankatsogolera magulu awo ankhondo a miyandamiyanda, Davide
ndi ankhondo ake ankayenda pambuyo pamodzi ndi Akisi. 3 Tsono
atsogoleri a Afilisti aja anafunsa kuti, "Kodi Ahebri awa akufuna chiyani?"

Akisi anayankha kuti, "Uyu ndi Davide, mtumiki wa Sauli mfumu ya Israeli. Iye wakhala ndi ine kwa masiku ndithu, kapena titi zaka ndipo kuyambira tsiku limene anachoka kwa Sauli mpaka lero, ine sindinapeze cholakwa mwa iye."

4 Koma atsogoleri a ankhondo a Afilisti anamukwiyira Akisi kwambiri
ndipo anati, "Mubweze munthuyu kuti abwerere ku malo amene unamupatsa. Iye asapite nafe ku nkhondo kuopa kuti angadzasanduke mdani wathu. Kodi iyeyu adzadziyanjanitsa bwanji ndi mbuye wake? Iyeyutu
adzadziyanjanitsa ndi mbuye wake pakupha anthu ali panowa? 5 Paja
ameneyu ndi Davide yemwe ankamuvinira namuyimbira kuti,

" 'Sauli wapha anthu 1,000
koma Davide wapha miyandamiyanda?' "

6 Kotero Akisi anayitana Davide ndipo anamuwuza kuti, "Pali Yehova
wamoyo, iwe wakhala wodalirika ndipo chikanakhala chinthu chabwino kuti uzimenya nkhondo pamodzi nane popeza chibwerere iwe kuno ine sindinapeze cholakwa chilichonse ndi iwe. Koma atsogoleri enawa ndiwo
sakukufuna. 7 Tsono bwerera. Upite mu mtendere kuopa kuti ungachite
kanthu kena koyipira atsogoleri a Afilistiwa."

8 Davide anafunsa Akisi kuti, "Kodi ndachita chiyani? Kodi mwapeza
cholakwa chotani mwa ine mtumiki wanu chiyambire kukutumikirani mpaka lero? Tsono chifukwa chiyani sindingapite kukamenya nkhondo ndi adani a mbuye wanga mfumu?"

9 Akisi anayankha kuti, "Ine ndikudziwa kuti ndiwe wangwiro ngati
mngelo wa Mulungu. Komabe atsogoleri a ankhondo a Afilisti akuti,
'Davide asapite nafe ku nkhondo.' 10 Tsono udzuke mmamawa, pamodzi
ndi ankhondo ako amene unabwera nawo, ndipo unyamuke kukangocha."

11 Choncho Davide ndi anthu ake anadzuka mmamawa kubwerera ku
dziko la Afilisti. Koma Afilistiwo anapita ku Yezireeli.

# 30

*Davide Amenyana ndi Aamaleki*

1 Pa tsiku lachitatu, Davide ndi anthu ake anakafika ku Zikilagi. Tsono
anapeza Aamaleki atawononga kale dera la Negevi ndi Zikilagi. Anathira
nkhondo mzinda wa Zikilagi ndi kuwutentha ndi moto. 2 Anatenga akazi
ndi onse amene anali m'menemo akuluakulu ndi ang'ono omwe kuti akakhale akapolo. Sanaphe aliyense koma anawatenga amoyo napita nawo.

3 Davide ndi anthu ake atafika ku Zikilagi anapeza kuti mzindawo
watenthedwa ndi moto ndipo akazi awo, ana awo, amuna ndi akazi
atengedwa ukapolo. 4 Kotero Davide ndi anthu ake analira mofuwula
mpaka analibenso mphamvu zolirira. 5 Akazi awiri a Davide, Ahinoamu
wa ku Yezireeli ndi Abigayeli mkazi wa Nabala wa ku Karimeli anatengedwanso. 6 Davide anavutika kwambiri mu mtima mwake chifukwa anthu
amakamba zoti amuponye miyala popeza aliyense anali ndi chisoni pokumbukira ana ake aamuna ndi aakazi. Koma Davide anapeza mphamvu mwa Yehova Mulungu wake.

7 Kenaka Davide anawuza wansembe Abiatara, mwana wa Ahimeleki
kuti, "Ndipatse efodi ija." Abiatara anabwera nayo efodiyo. 8 Tsono Davide

anapempha nzeru kwa Yehova nati, “Kodi ndilitsatire gulu lankhondoli? Kodi ndidzawapambana?”

Yehova anayankha kuti, “Litsatire, iwe udzawapambana ndithu ndipo udzapulumutsa anthu ako.”

9 Davide pamodzi ndi anthu ake 600 aja ananyamuka nafika ku mtsinje
wa Besori. Kumeneko anasiyako anthu ena. 10 Davide ndi anthu ake
400 anapitirira kuwalondola Aamaleki aja. Koma anthu ena 200 anatsala popeza anatopa moti sakanatha kuwoloka mtsinje wa Besori uja.

11 Anthu amene anali ndi Davide anapeza Mwigupto m'munda wina
ndipo anabwera naye kwa Davide. Iwo anamupatsa madzi kuti amwe
ndi chakudya kuti adye. 12 Anamupatsanso chidutswa cha keke yankhuyu
ndi makeke awiri a mphesa zowumika kuti adye. Atadya anapezanso mphamvu popeza anakhala masiku atatu wosadya kapena kumwa kanthu kalikonse.

13 Davide anafunsa kuti, “Kodi ndiwe yani, ndipo ukuchokera kuti?”

Iye anayankha kuti, “Ine ndine Mwigupto, kapolo wa Mwamaleki. Mbuye wanga anandisiya nditayamba kudwala masiku atatu apitawo.
14 Ife tinathira nkhondo dera la kummwera kwa mayiko a Akereti, dera la Yuda, ndi dera la kummwera kwa mayiko a Kalebe. Mzinda wa Zikilagi tinawutentha ndi moto.”

15 Davide anamupempha kuti, “Kodi unganditsogolere kumene kuli gulu lankhondoli?”

Iye anayankha kuti, “Mukandilonjeza molumbira kuti simudzandipha kapena kundipereka kwa mbuye wanga, ine ndikulondolerani kumene kuli gululo.”

16 Mwigupto uja anaperekeza Davide. Tsono Aamaleki anali
atamwazikana ponseponse. Iwo ankadya, kumwa ndi kuvina chifukwa cha zofunkha zambiri zimene anatenga ku dziko la Afilisti ndi ku dziko la
Ayuda. 17 Tsono Davide anawakantha kuyambira madzulo atsikulo mpaka
madzulo a tsiku linalo. Palibe anapulumuka kupatula anyamata 400
amene anakwera pa ngamira n'kuthawa. 18 Choncho Davide analanditsa
zinthu zonse zimene Aamaleki aja anatenga. Anapulumutsanso akazi
ake awiri aja. 19 Palibe chimene chinasowa anthu onse, kuyambira wamng'ono mpaka wamkulu, mnyamata mpaka mtsikana anapulumutsidwa. Davide anapulumutsa chilichonse chimene anafunkha Aamaleki
aja. 20 Anapulumutsanso nkhosa ndi ng'ombe zonse. Tsono anthu ankakusa ziwetozo namati, “Izi ndizo zofunkha za Davide.”

21 Davide anafika ku malo kumene kunali anthu 200 otopa kwambiri
aja amene sanathe kutsagana naye koma anangokhala ku mtsinje wa Besori. Tsono ananyamuka kuti akumane ndi Davide pamodzi ndi
anthu amene anali naye. Davide anawayandikira nawalonjera. 22 Tsono
anthu ena oyipa mtima achabechabe mwa amene anatsagana ndi Davide aja anati, “Popeza awa sanapite nafe, sitiwapatsako zofunkha zimene tapulumutsazi, kupatula kuti aliyense atenge mkazi wake ndi ana ake azipita.”

23 Koma Davide anawayankha kuti, “Ayi, abale anga, musachite
zimenezi ndi zinthu zimene Yehova watipatsa. Iye watisunga ndi kupereka m'manja mwathu gulu la ankhondo limene linabwera kudzalimbana
nafe. 24 Ndani angakumvereni zimene mukunenazi? Gawo la munthu
amene anapita kukamenya nkhondo likhale lofanana ndi la munthu amene anatsala pano kuyang'anira katundu wathu. Pasakhale kusiyana

kulikonse.” 25 Choncho Davide anakhazikitsa ngati lamulo m’chitidwe
woterewu pakati pa Aisraeli kuyambira tsiku limenelo mpaka lero.

26 Davide atafika ku Zikilagi, anatumiza zina mwa zofunkhazo kwa
akuluakulu a Yuda, amene anali abwenzi ake. Anati, “Nayi mphatso yanu
yochokera pa zofunkha za adani a Yehova.”

27 Iye anatumiza mphatsozo kwa anthu a ku Beteli, Ramoti-Negavi,
Yatiri, 28 Aroeri, Sifimoti, Esitemowa 29 Rakala, mizinda ya fuko la
Ayerahimeeli, mizinda ya fuko la Akeni, 30 a ku Horima, Borasani, Ataki,
31 Hebroni pamodzi ndi onse a kumalo kumene Davide ndi anthu ake
anakhala akuyendayendako.

# 31

*Imfa ya Sauli ndi Ana Ake*

1 Tsono Afilisti anachitanso nkhondo ndi Aisraeli ndipo Aisraeli
anathawa Afilistiwo, kotero kuti ambiri anaphedwa pa phiri la Gilibowa.
2 Afilisti anapanikiza kwambiri Sauli ndi ana ake, ndipo anapha Yonatani,
Abinadabu ndi Maliki-Suwa. 3 Nkhondo inakula kwambiri mozungulira
Sauli ndipo pamene anthu amauta anamupeza, anamuvulaza kwambiri.

4 Tsono Sauli anawuza mnyamata wake wonyamula zida zake kuti,
“Solola lupanga lako undiphe kuopa kuti anthu osachita mdulidwewa
angabwere kudzandizunza ine.”

Koma mnyamata wonyamula zida uja anachita mantha kwambiri ndipo
sanathe kutero. Choncho Sauli anatenga lupanga lake lomwe nagwerapo.
5 Mnyamata wonyamula zida zake uja ataona kuti Sauli wafa, nayenso
anadzigwetsera pa lupanga lake nafa naye limodzi. 6 Motero Sauli ndi
ana ake atatu, wonyamula zida zake pamodzi ndi anthu ake onse anafera
limodzi pa tsikulo.

7 Pamene Aisraeli amene anali tsidya lina la chigwa ndi amene anali
tsidya la chigwa cha Yorodani anaona kuti gulu la ankhondo la Aisraeli
lathawa komanso kuti Sauli ndi ana ake aphedwa, nawonso anathawa
kusiya mizinda yawo. Ndipo Afilisti anabwera kudzakhalamo.

8 Mmawa mwake, Afilisti atabwera kudzatenga zinthu za anthu
ophedwa anapeza Sauli ndi ana ake atatu atafa pa phiri la Gilibowa. 9 Iwo
anadula mutu wake ndi kumuvula zida zake zankhondo. Ndipo anatumiza
amithenga m’dziko lonse la Afilisti kukafalitsa nkhani yabwinoyi kwa
mafano awo ndi kwa anthu awo. 10 Iwo anayika zida zake zankhondo
m’nyumba yopembedzera Asitoreti, ndipo thupi lake analikhomera pa
khoma la mzinda wa Beti-Sani.

11 Pamene anthu a ku Yabesi Giliyadi anamva zimene Afilisti anachitira
Sauli, 12 anthu awo onse olimba mtima anayenda usiku wonse kupita ku
Beti-Sani. Anakachotsa mtembo wa Sauli ndi mitembo ya ana ake pa
khoma la mzinda wa Beti-Sani, ndipo anabwera nayo ku Yabesi kumene
anayitentha ndi moto. 13 Pambuyo pake anatenga mafupa awo ndi
kuwakwirira pansi pa mtengo wabwemba ku Yabesi, ndipo anasala kudya
masiku asanu ndi awiri.

# 2 Samueli

### *Davide Amva za Imfa ya Sauli*

1 Atamwalira Sauli, Davide anabwerako kumene anakagonjetsa Aa-
maleki ndipo anakakhala ku Zikilagi masiku awiri. 2 Pa tsiku lachitatu
munthu wina wochokera ku msasa wa Sauli anafika, zovala zake
zitang'ambika ndiponso anali atathira dothi pamutu pake. Atafika kwa
Davide, anadzigwetsa pansi, kupereka ulemu kwa Davideyo.
3 Davide anamufunsa iye kuti, "Kodi iwe wachokera kuti?"
Iye anayankha kuti, "Ine ndathawa ku misasa ya Aisraeli."
4 Davide anafunsa, "Tandiwuza, chachitika ndi chiyani?"
Iye anati, "Anthu athawa ku nkhondo ndipo ambiri aphedwa. Sauli ndi
mwana wake Yonatani aphedwa."
5 Ndipo Davide anati kwa mnyamata amene anabweretsa nkhaniyi,
"Ukudziwa bwanji kuti Sauli ndi mwana wake Yonatani afa?"
6 Mnyamatayo anati, "Zinangochitika kuti ndinali pa phiri la Gilibowa,
ndipo Sauli anali komweko ataweramira pa mkondo wake, pamodzi ndi
magaleta ndi okwera ake atamuyandikira. 7 Pamene anatembenuka ndi
kundiona ine, iye anandiyitana, ndipo ndinati, 'Kodi ndichite chiyani?' "
8 Iye anandifunsa, "Iwe ndiwe yani?"
Ine ndinayankha kuti, "Ndine Mwamaleki."
9 "Kenaka iye anati kwa ine, 'Bwera pafupi ndipo undiphe! Ndikumva
ululu kwambiri, koma ndikanali ndi moyo!'
10 "Kotero ndinabwera pafupi ndi kumupha, chifukwa ndinadziwa kuti
mmene anagweramo sakanakhalanso ndi moyo. Ndipo ndatenga chipewa
chaufumu chimene chinali pamutu pake ndi khoza la pa dzanja lake ndipo
ndazibweretsa kwa inu mbuye wanga."
11 Apo Davide ndi anthu onse amene anali nawo anang'amba zovala
zawo. 12 Iwo analira maliro ndi kusala zakudya mpaka madzulo chifukwa
cha Sauli ndi mwana wake Yonatani, komanso chifukwa cha gulu la
ankhondo la Yehova ndi nyumba ya Israeli, chifukwa anaphedwa ndi
lupanga.
13 Davide anati kwa mnyamata amene anabweretsa uthengawo, "Iwe
umachokera kuti?"
Iye anayankha kuti, "Ine ndine mwana wa mlendo Mwamaleki."
14 Davide anamufunsanso kuti, "N'chifukwa chiyani sunaope kukweza
dzanja lako ndi kupha wodzozedwa wa Yehova?"
15 Kenaka Davide anayitana mmodzi mwa anyamata ake ndipo anati,
"Pita ukamukanthe!" Kotero iye anapita kukamukantha, ndipo mnyamata
uja anafa. 16 Pakuti Davide anali atanena kwa iye kuti, "Iwe wadzipha
wekha. Pakamwa pako pakunena zokutsutsa wekha, pamene unanena
kuti, 'Ine ndapha wodzozedwa wa Yehova.' "

### *Davide Alira Maliro a Sauli ndi Yonatani*

17 Davide anayimba nyimbo iyi ya maliro, kulira Sauli ndi mwana wake
Yonatani. 18 Ndipo analamula kuti anthu a ku Yuda aphunzitsidwe nyimbo
ya maliroyi imene yalembedwa m'buku la Yasari:
19 "Ulemerero wako iwe Israeli, wagona utaphedwa ku zitunda.
Taonani amphamvu agwa kumeneko!

20 “Musakanene zimenezi ku Gati,
musazilengeze ku misewu ya ku Asikeloni,
kuti ana aakazi a Afilisti angasangalale,
ana aakazi a osachita mdulidwe angakondwere.

21 “Inu mapiri a ku Gilibowa,
musakhalenso ndi mame kapena mvula,
kapena minda yobereka zopereka za ufa.
Pakuti kumeneko chishango cha munthu wamphamvu chinadetsedwa,
chishango cha Sauli sanachipakenso mafuta.

22 “Pa magazi a ophedwa,
pa mnofu wa amphamvu,
uta wa Yonatani sunabwerere,
lupanga la Sauli silinabwere chabe.

23 “Sauli ndi Yonatani,
pa moyo wawo anali okondedwa ndi okoma mtima,
ndipo pa imfa yawo sanasiyanitsidwe.
Iwo anali ndi liwiro loposa ziwombankhanga,
anali ndi mphamvu zoposa mkango.

24 “Inu ana aakazi a Israeli,
mulireni Sauli,
amene anakuvekani zovala zofiira ndi zofewa,
amene anakometsera zovala zanu ndi zokometsera zagolide.

25 “Taonani amphamvu agwa ku nkhondo!
Yonatani wagona ataphedwa ku zitunda.
26 Ine ndikuvutika mumtima chifukwa cha iwe m’bale wanga Yonatani,
unali wokondedwa kwambiri kwa ine.
Chikondi chako pa ine chinali chopambana,
chopambana kuposa chikondi cha akazi.

27 “Taonani amphamvu agwa!
Zida zankhondo zawonongeka!”

# 2

### *Davide Adzozedwa Kukhala Mfumu ya Yuda*

1 Patapita nthawi, Davide anafunsa Yehova kuti, “Kodi ndipite ku umodzi mwa mizinda ya Yuda?”

Yehova anayankha kuti, “Pita.”

Davide anafunsanso kuti, “Kodi ndipite kuti?”

Yehova anayankha kuti, “Ku Hebroni.”

2 Choncho Davide anapita kumeneko ndi akazi ake awiri, Ahinoamu wa
ku Yezireeli ndi Abigayeli mkazi wamasiye uja wa Nabala wa ku Karimeli.
3 Davide anatenganso anthu amene anali nawo aliyense ndi banja lake,
ndipo anakakhala ku midzi ya ku Hebroni. 4 Kenaka amuna a ku Yuda
anabwera ku Hebroni ndipo kumeneko anadzoza Davide kukhala mfumu
ya fuko la Yuda.

Davide atawuzidwa kuti anthu a ku Yabesi Giliyadi ndi amene anayika
m'manda Sauli, 5 iye anatuma amithenga kwa anthu a ku Yabesi Giliyadi
kuti akayankhule nawo kuti, "Yehova akudalitseni poonetsa kukoma
mtima kwanu kwa Sauli mbuye wanu pomuyika m'manda. 6 Tsopano
Yehova akuonetseni kukoma mtima ndi kukhulupirika kwake ndipo in-
enso ndidzakukomerani mtima chifukwa munachita zimenezi. 7 Tsopano
khalani amphamvu ndi olimba mtima, pakuti Sauli mbuye wanu wafa,
ndipo fuko la Yuda landidzoza kukhala mfumu yawo."

### *Nkhondo Pakati pa Otsatira Davide ndi Otsatira Sauli*

8 Pa nthawi imeneyi Abineri mwana wa Neri, wolamulira ankhondo
a Sauli, anatenga Isi-Boseti mwana wa Sauli ndi kubwera naye ku
Mahanaimu. 9 Iye anamuyika kuti akhale mfumu yoyang'anira Giliyadi,
Asuri ndi Yezireeli, pamodzi ndi Efereimu, Benjamini ndi Israeli yense.

10 Isi-Boseti mwana wa Sauli anali wa zaka makumi anayi pamene
anakhala mfumu ya Israeli ndipo analamulira zaka ziwiri. Koma fuko
la Yuda linatsatira Davide. 11 Davide anakhala mfumu ku Hebroni
akulamulira fuko la Yuda, kwa zaka zisanu ndi chimodzi ndi miyezi isanu
ndi umodzi.

12 Abineri mwana wa Neri, pamodzi ndi ankhondo a Isi-Boseti mwana
wa Sauli, anachoka ku Mahanaimu ndi kupita ku Gibiyoni. 13 Yowabu
mwana wa Zeruya pamodzi ndi ankhondo a Davide anapita ndi kukaku-
mana nawo ku dziwe la ku Gibiyoni. Gulu lina linakhala mbali ina ya
dziwelo pamene gulu lina linakhala mbali inayo.

14 Kenaka Abineri anati kwa Yowabu, "Tiye tibweretse ena mwa
anyamata athu kuti amenyane patsogolo pathupa."

Yowabu anayankha, "Chabwino, amenyane."

15 Kotero anayimirira ndipo anawawerenga: anyamata khumi ndi
awiri a fuko la Benjamini ndi Isi-Boseti mwana wa Sauli ndiponso
anyamata khumi ndi awiri a Davide. 16 Tsono aliyense anagwira mutu wa
mnzake namubaya mnzakeyo m'nthiti ndi mpeni ndipo onse anagwera
pansi limodzi. Kotero malo amenewo ku Gibiyoni amatchedwa Helikati
Hazurimu.

17 Tsiku limeneli nkhondo yake inali yoopsa kwambiri, ndipo Abineri
ndi ankhondo a Israeli anagonjetsedwa ndi ankhondo a Davide.

18 Ana atatu aamuna a Zeruya, Yowabu, Abisai ndi Asaheli anali
komweko. Koma Asaheli anali waliwiro ngati insa. 19 Iye anathamangitsa
Abineri ndipo sanakhotere kumanja kapena kumanzere pamene amamut-
satira. 20 Abineri anayang'ana m'mbuyo ndipo anafunsa, "Kodi ndiwe
Asaheli?"

Iye anayankha kuti, "Ndine."

21 Ndipo Abineri anati kwa iye, "Khotera kumanja kapena kumanzere:
tsatira mmodzi mwa anyamatawa ndipo umulande zida zake." Koma
Asaheli sanasiye kumuthamangitsa.

22 Abineri anamuchenjezanso Asaheli, "Siya kuthamangitsa ine! Kodi
ndikukanthe chifukwa chiyani? Kodi ndikaonana naye bwanji m'bale
wako Yowabu?"

23 Koma iye anakana kuleka kumuthamangitsa. Choncho Abineri
anabaya Asaheli m'mimba ndi msonga ya mkondo wake ndipo mkondowo
unatulukira mbali ina. Iye anagwa ndi kufera pamalo pomwepo. Ndipo
munthu aliyense amayima akafika pamalo pamene anagwera ndi kufa.

24 Koma Yowabu ndi Abisai anathamangitsa Abineri, ndipo dzuwa likulowa, anafika ku phiri la Ama, pafupi ndi Giya pa njira yopita ku
chipululu cha ku Gibiyoni.
25 Pamenepo anthu a fuko la Benjamini anasonkhana kudzathandiza Abineri. Iwo anapanga gulu ndipo anayima pamwamba pa phiri.

26 Abineri anayitana Yowabu, "Kodi tipitirize kumenyana mpaka kalekale? Kodi sukuzindikira kuti mathero ake kudzakhala kuwawidwa mitima? Kodi udzawaletsa liti ankhondo ako kuthamangitsa abale awo?"

27 Yowabu anayankha kuti, "Pali Yehova wamoyo, ukanapanda kuyankhula, ankhondo anga akanapitiriza kuthamangitsa abale awo mpaka mmawa."

28 Chomwecho Yowabu analiza lipenga, ndipo ankhondo onse anayima. Iwo analeka kuthamangitsa Aisraeli kapena kumenyana nawo.

29 Usiku wonsewo Abineri ndi ankhondo ake anayenda kudutsa Araba. Iwo anawoloka Yorodani, napitirira mpaka kudutsa dera lonse la Bitironi ndipo anafika ku Mahanaimu.

30 Choncho Yowabu anabwerera kuchokera kothamangitsa Abineri ndipo anasonkhanitsa ankhondo ake onse. Kupatula Asaheli, panali
ankhondo khumi ndi anayi a Davide amene anasowa.
31 Koma ankhondo
a Davide anapha ankhondo a fuko la Benjamini 360 amene anali ndi
Abineri.
32 Iwo anatenga Asaheli ndi kukamuyika m'manda a abambo ake ku Betelehemu. Ndipo Yowabu ndi ankhondo ake anayenda usiku wonse ndi kufika ku Hebroni kukucha.

# 3

1 Nkhondo ya pakati pa banja la Sauli ndi banja la Davide inachitika nthawi yayitali. Mphamvu za Davide zinkakulirakulirabe, pamene banja la Sauli mphamvu zake zimapita zicheperachepera.

2 Ana aamuna a Davide amene anabadwira ku Hebroni anali awa:
Woyamba anali Amnoni, amayi ake anali Ahinoamu wa ku Yezireeli.
3 Mwana wachiwiri anali Kileabu, amayi ake anali Abigayeli mkazi wamasiye wa Nabala wa ku Karimeli.
Wachitatu anali Abisalomu, amayi ake anali Maaka mwana wa Talimai mfumu ya Gesuri;
4 wachinayi anali Adoniya, amayi ake anali Hagiti;
wachisanu, Sefatiya amayi ake anali Abitali;
5 ndipo wachisanu ndi chimodzi anali Itireamu, amayi ake anali Egila, mkazi wa Davide.
Ana awa a Davide anabadwira ku Hebroni.

### *Abineri Agwirizana ndi Davide*

6 Pamene kunali nkhondo pakati pa banja la Sauli ndi banja la Davide, Abineri anayamba kudzipatsa yekha mphamvu pakati pa banja la Sauli.
7 Sauli anali ndi mzikazi dzina lake Rizipa mwana wa Ayiwa. Ndipo Isiboseti anati kwa Abineri, "N'chifukwa chiyani unagona ndi mzikazi wa abambo anga?"

8 Abineri anakwiya kwambiri chifukwa cha zimene Isi-Boseti ananena ndipo anamuyankha kuti "Kodi ukuyesa ndine mutu wagalu umene ali mbali ya Ayuda? Lero lino ndine wokhulupirika ku nyumba ya abambo ako, Sauli ndi banja lake ndi anzake. Ine sindinakupereke kwa Davide, koma tsopano ukundinena pa cholakwa chimene ndachita pa mkazi uyu!
9 Mulungu andilange ine Abineri, andilange kwambiri, ngati sindichitira

Davide zimene Yehova anamulonjeza iye mwa lumbiro. 10 Ndidzachotsa
ufumu ku nyumba ya Sauli ndi kukhazikitsa ufumu wa Davide pa Aisraeli
onse ndi Yuda kuchokera ku Dani mpaka ku Beeriseba.” 11 Isiboseti
sanayerekezenso kunena mawu ena kwa Abineri, chifukwa ankamuopa.

12 Kenaka Abineri anatuma amithenga kwa Davide kukanena kuti, “Kodi
dzikoli ndi la yani? Uchite mgwirizano ndi ine ndipo ndidzakuthandiza
kuti Aisraeli onse azikutsatira.”

13 Davide anati, “Chabwino. Ine ndichita mgwirizano ndi iwe. Koma
ndikukupempha chinthu chimodzi: Usabwere pamaso panga pokhapokha
utabweretsa Mikala mwana wamkazi wa Sauli, ukamabwera kudzan-
diona.” 14 Ndipo Davide anatuma amithenga kwa Isi-Boseti mwana wa
Sauli, kumulamula kuti, “Patse mkazi wanga Mikala, amene ndinamuk-
watira ndi makungu 100 a msonga za mavalo a Afilisti.”

15 Kotero Isi-Boseti analamulira ndipo anakamutenga kwa mwamuna
wake Palitieli mwana wa Laisi. 16 Koma mwamuna wake anapita naye
akulira pambuyo pake njira yonse mpaka ku Bahurimu. Kenaka Abineri
anati kwa iye, “Bwerera kwanu!” Ndipo anabwerera kwawo.

17 Abineri anakambirana ndi akuluakulu a Israeli ndipo anati, “Kwa
kanthawi mwakhala mukufuna kulonga Davide kuti akhale mfumu yanu.
18 Tsopano chitani zimenezo! Pakuti Yehova analonjeza Davide kuti,
‘Kudzera mwa mtumiki wanga Davide ndidzapulumutsa anthu anga
Aisraeli m’dzanja la Afilisti ndi kuwachotsa m’manja mwa adani awo.’ ”

19 Abineri anayankhulanso nawo yekha anthu a fuko la Benjamini.
Kenaka anapita ku Hebroni kukamuwuza Davide zonse zimene Aisraeli
ndi fuko lonse la Benjamini amafuna kuchita. 20 Abineri, amene anali
ndi anthu makumi awiri, atafika kwa Davide ku Hebroni, Davide ana-
mukonzera phwando pamodzi ndi anthu ake. 21 Ndipo Abineri anawuza
Davide kuti, “Loleni kuti ndipite msanga kukasonkhanitsa Aisraeli onse
kuti abwere kwa inu kuno, mbuye wanga mfumu, kuti adzachite nanu
pangano, ndipo kuti muzilamulira kulikonse kumene mtima wanu ufuna.”
Kotero Davide analola Abineri kuti apite, ndipo anapita mwamtendere.

### *Yowabu Apha Abineri*

22 Nthawi yomweyo ankhondo a Davide ndi Yowabu anafika kuchok-
era kumene anakathira nkhondo ndipo anabweretsa katundu wambiri
wolanda ku nkhondo. Koma Abineri sanalinso ndi Davide ku Hebroni,
chifukwa Davide anamulola kuti apite, ndipo anapita mu mtendere.
23 Yowabu ndi asilikali onse amene anali naye atafika, anawuzidwa
kuti Abineri mwana wa Neri anabwera kwa mfumu ndipo kuti mfumu
yamulola kuti apite ndi kuti wapita ndi mtendere.

24 Choncho Yowabu anapita kwa mfumu ndipo anati, “Mwachita
chiyani? Taonani, Abineri anabwera kwa inu. N’chifukwa chiyani
mwamulola kuti apite? Tsopanotu wapitadi! 25 Inu mukumudziwa bwino
Abineri mwana wa Neri. Iye anabwera kudzakunamizani ndi kudzaona
mayendedwe anu ndiponso kudzaona zonse zimene mukuchita.”

26 Kenaka Yowabu anachoka pamaso pa Davide ndipo anatumiza
amithenga kutsatira Abineri, ndipo anabwera naye kuchokera ku chitsime
cha Sira. Koma Davide sanadziwe zimenezi. 27 Tsono Abineri atabwerera
ku Hebroni, Yowabu anamutengera pambali ku chipata, kukhala ngati
akufuna kuyankhula naye mwamseri. Ndipo kumeneko pobwezera imfa
ya m’bale wake Asaheli, Yowabu analasa iyeyo m’mimba, ndipo anafa.

28 Patapita nthawi, Davide atamva zimenezi anati, “Ine ndi ufumu
wanga tidzakhala osalakwa pamaso pa Yehova pa imfa ya Abineri mwana
wa Neri. 29 Mlandu umenewu ukhala pa Yowabu ndi banja lonse
la abambo ake! M’banja la Yowabu musadzasowe munthu wodwala
matenda a chizonono kapena khate, kapena wolumala woyendera ndodo
kapena wophedwa ndi lupanga, kapena wosowa chakudya.”

30 (Yowabu ndi m’bale wake Abisai anapha Abineri chifukwa iye anapha
m’bale wawo Asaheli ku nkhondo ku Gibiyoni).

31 Ndipo Davide anati kwa Yowabu ndi anthu onse amene anali nawo,
“Ng’ambani zovala zanu ndipo muvale ziguduli, muyende mukulira patso-
golo pa Abineri.” Mfumu Davide mwini anayenda motsatira chitandacho.
32 Iwo anamuyika Abineri m’manda ku Hebroni ndipo mfumu inalira
mokweza pa manda a Abineri. Ndipo anthu onse analiranso.

33 Mfumu inayimba nyimbo iyi ya maliro a Abineri:

“Abineri n’kufa motere monga mmene chimafera chitsiru.
34 Manja ako anali osamanga,
mapazi ako anali osakulungidwa.
Iwe wafa monga mmene amafera anthu pamaso pa anthu oyipa.”

Ndipo anthu onse analiranso kulirira Abineri.

35 Kenaka onse anabwera kwa Davide kumuwumiriza kuti adye
kusanade. Koma Davide analumbira kuti, “Mulungu andilange ine,
andilange kwambiri, ngati ndilawe buledi kapena chilichonse dzuwa
lisanalowe!”

36 Anthu onse anadziwa zimenezi ndipo zinawakondweretsa ndithu.
Zonse zimene mfumu inachita zinawakondweretsa. 37 Kotero tsiku
limeneli anthu onse ndi Aisraeli onse anadziwa kuti sikunali kufuna kwa
mfumu kuti Abineri mwana wa Neri aphedwe.

38 Ndipo mfumu inati kwa ankhondo ake, “Kodi inu simukudziwa kuti
lero mu Israeli mwagwa kalonga ndi munthu wamkulu? 39 Ndipo lero,
ngakhale ine ndine mfumu yodzozedwa, ndilibe mphamvu ndipo ana awa
a Zeruya ndi amphamvu kwa ine. Yehova abwezere woyipa molingana ndi
zoyipa zake!”

# 4

*Kuphedwa kwa Isiboseti*

1 Isiboseti mwana wa Sauli atamva kuti Abineri waphedwa ku Hebroni,
anataya mtima ndipo Aisraeli onse anachita mantha kwambiri. 2 Koma
Isiboseti anali ndi anthu akuluakulu awiri amene ankatsogolera magulu
a ankhondo. Mmodzi mwa iwo dzina lake linali Baana ndipo mnzakeyo
anali Rekabu. Iwo anali ana a Rimoni wa banja la Beeroti wa fuko la
Benjamini Beeroti. Iwo ankatengedwa ngati mbali imodzi ya Benjamini,
3 chifukwa anthu a ku Beeroti anathawira ku Gitaimu ndipo akhala ali
kumeneko ngati alendo mpaka lero lino.

4 (Yonatani mwana wa Sauli anali ndi mwana wamwamuna amene anali
wolumala mapazi ake onse awiri. Iye anali ndi zaka zisanu pamene
nkhani ya Sauli ndi Yonatani inamveka kuchokera ku Yezireeli. Amene
amamulera anamunyamula ndi kuthawa naye, koma pamene amachita
zinthu mofulumira mwanayo anagwa ndipo analumala. Dzina lake linali
Mefiboseti).

5 Choncho Rekabu ndi Baana ana a Rimoni wa ku Beeroti ananyamuka
kupita ku nyumba ya Isi-Boseti, ndipo anafika nthawi ya masana kukuten-
tha pamene iye amapumula. 6 Iwo analowa m'chipinda cham'kati ngati
kuti amakatenga tirigu, ndipo anamulasa m'mimba. Kenaka Rekabu ndi
m'bale wake Baana anathawa.
7 Iwo analowa m'nyumbamo iye akugona pa bedi m'chipinda chake.
Atamulasa ndi kumupha, anadula mutu wake n'kuwutenga, nayenda
usiku wonse m'njira yopita ku Araba. 8 Iwo anabweretsa mutu wa Isi-
Boseti kwa Davide ku Hebroni ndipo anati kwa mfumu, "Nawu mutu wa
Isiboseti mwana wa Sauli, mdani wanu, amene anafuna kukuphani. Lero
lino Yehova wabwezera mbuye wanga mfumu adani anu, Sauli ndi ana
ake."
9 Davide anayankha Rekabu ndi m'bale wake Baana, ana a Rimoni
wa ku Beeroti kuti, "Pali Yehova wamoyo, amene wandipulumutsa ku
mavuto anga onse, 10 pamene munthu wina anandiwuza kuti, 'Sauli wafa'
ndipo ankaganiza kuti wabweretsa nkhani yabwino, ine ndinamugwira
ndi kumupha ku Zikilagi. Iyi inali mphotho imene ndinapereka kwa
iyeyo chifukwa cha uthenga wake! 11 Nanji pamene anthu oyipa apha
munthu wosalakwa ali m'nyumba mwake ndiponso pa bedi lake! Kodi
ine ndingaleke kukulangani ndi kukuchotsani pa dziko lapansi pano?"
12 Kotero Davide analamulira ankhondo ake, ndipo anawapha. Iwo
anawadula manja ndi mapazi ndi kupachika matupi awo pa dziwe la ku
Hebroni. Koma anatenga mutu wa Isi-Boseti nawuyika m'manda a Abineri
ku Hebroni.

# 5

### *Davide Adzozedwa Kukhala Mfumu ya Israeli*

1 Mafuko onse a Israeli anabwera kwa Davide ku Hebroni ndipo anati,
"Ife ndife mafupa ndi mnofu wanu. 2 Kale lija, pamene Sauli anali
mfumu yathu, inu ndinu amene munkatsogolera Aisraeli pa nkhondo
zawo. Ndipo Yehova anakuwuzani kuti, 'Udzaweta anthu anga Aisraeli,
ndipo udzakhala mfumu yawo.' "
3 Akuluakulu onse a Israeli atafika kwa Mfumu Davide ku Hebroni,
mfumu inachita nawo pangano ku Hebroni pamaso pa Yehova, ndipo
anamudzoza Davide kukhala mfumu ya Israeli.
4 Davide anali ndi zaka makumi atatu pamene anakhala mfumu, ndipo
analamulira zaka makumi anayi. 5 Analamulira Yuda ali ku Hebroni
kwa zaka zisanu ndi ziwiri ndi miyezi isanu ndi umodzi, ndipo ali ku
Yerusalemu analamulira Israeli yense ndi Yuda kwa zaka 33.

### *Davide Alanda Mzinda wa Yerusalemu*

6 Mfumu ndi ankhondo ake anapita ku Yerusalemu kukathira nkhondo
Ayebusi amene ankakhala kumeneko. Ayebusiwo anamuwuza Davide
kuti, "Inu simulowa muno. Ngakhale osaona ndi olumala akhoza
kukuthamangitsani." Iwo ankaganiza kuti, "Davide sangathe kulowa
momwemo." 7 Komabe Davide analanda linga la Ziyoni, limene ndi
mzinda wa Davide.
8 Pa tsiku limenelo Davide anati, "Aliyense wogonjetsa Ayebusi ayenera
kudzera m'ngalande ya madzi kuti akafike kwa iwo amene ndi 'olumala
ndi osaona,' amene ndi adani a Davide." N'chifukwa chake amanena kuti,
"Olumala ndi osaona sadzalowa m'nyumba yaufumu."

9 Tsono Davide anakhazikika mu lingamo ndipo mzindawu anawutcha,
Mzinda wa Davide. Iye anamanga malo onse ozungulira kuyambira ku
matsitso ozungulira khoma. 10 Ndipo mphamvu za Davide zinkakuli-
rakulira chifukwa anali ndi Yehova Mulungu Wamphamvuzonse.
11 Tsono Hiramu mfumu ya Turo inatumiza amithenga ake kwa Davide,
pamodzi ndi mitengo ya mkungudza ndi amisiri a matabwa ndi amisiri
a miyala, ndipo anamumangira Davide nyumba yaufumu. 12 Choncho
Davide anazindikira kuti Yehova wamukhazikitsa kukhala mfumu ya
Israeli ndipo wakuza ufumu wake chifukwa cha anthu ake, Aisraeli.
13 Davide atafika ku Yerusalemu kuchokera ku Hebroni, anakwatira
azikazi natenganso akazi ena kumeneko, ndipo anabereka ana aamuna
ndi aakazi ambiri. 14 Mayina a ana amene anabereka ku Yerusalemu ndi
awa: Samua, Sobabu, Natani, Solomoni, 15 Ibihari, Elisua, Nefegi, Yafiya,
16 Elisama, Eliada ndi Elifeleti.

### *Davide Agonjetsa Afilisti*

17 Afilisti atamva kuti Davide wadzozedwa kukhala mfumu ya Israeli,
iwo anapita mwamphamvu kukamusakasaka. Koma Davide atamva
zimenezi anakalowa mu linga. 18 Ndipo Afilisti anabwera ndi kukhala
momwazika m'Chigwa cha Refaimu. 19 Davide anafunsa Yehova kuti,
"Kodi ndipite kukathira nkhondo Afilisti? Kodi mukawapereka m'manja
mwanga?"
Yehova anamuyankha kuti, "Pita, Ine ndidzawapereka ndithu m'manja
mwako."
20 Choncho Davide anapita ku Baala-Perazimu ndi kugonjetsa Afilistiwo.
Iye anati, "Monga amasefukira madzi, Yehova waphwanya adani anga
ine ndikuona." Choncho anawatcha malowa Baala Perazimu. 21 Afilisti
anasiya mafano awo kumeneko ndipo Davide ndi ankhondo ake anawa-
tenga.
22 Nthawi inanso Afilisti anabweranso namwazikana m'Chigwa cha
Refaimu; 23 Davide anafunsa Yehova ndipo Yehovayo anayankha kuti,
"Usapite molunjika koma uzungulire kumbuyo kwawo ndipo ukawathire
nkhondo patsogolo pa mitengo ya mkandankhuku. 24 Mukakangomva
phokoso pa msonga za mitengo ya mkandankhuku, mukayende mo-
fulumira, chifukwa izi zikasonyeza kuti Yehova ali patsogolo panu
kukantha ankhondo a Afilisti." 25 Kotero Davide anachita zimene Yehova
anamulamulira ndipo anakantha Afilisti njira yonse kuchokera ku Geba
mpaka ku Gezeri.

## 6

### *Bokosi la Chipangano Libwera ku Yerusalemu*

1 Davide anasonkhanitsanso pamodzi ankhondo 3,000 osankhidwa
pakati pa Aisraeli. 2 Iye pamodzi ndi ankhondo ake onse anapita ku
Baalahi ku Yuda kukatenga Bokosi la Chipangano la Mulungu, limene
limadziwika ndi Dzina lake, dzina la Yehova Wamphamvuzonse, amene
amakhala pakati pa Akerubi amene ali pa Bokosi la Chipanganolo. 3 Iwo
anayika Bokosi la Mulungu pa ngolo yatsopano nachoka nalo ku nyumba
ya Abinadabu, imene inali pa phiri. Uza ndi Ahiyo ana a Abinadabu ndiwo
ankayendetsa ngolo yatsopanoyo, 4 imene inanyamula Bokosi la Mulungu,
ndipo Ahiyo mwana wa Abinadabu ankayenda patsogolo pake. 5 Davide
pamodzi ndi Aisraeli onse ankakondwerera ndi mphamvu zawo zonse

pamaso pa Yehova poyimba nyimbo pogwiritsa ntchito azeze, apangwe, matambolini, maseche ndi malipenga.

6 Atafika pa malo opunthira tirigu a Nakoni, Uza anatambalitsa dzanja lake kuti agwire Bokosi la Mulungu, chifukwa ng'ombe zinkafuna kugwa.
7 Yehova anapsera mtima Uza chifukwa chochita chinthu chosayenera kuchitika. Choncho Mulungu anamukantha ndipo anafera pomwepo pambali pa Bokosi la Mulungulo.

8 Ndipo Davide anakhumudwa chifukwa Yehova anakantha Uza ndipo mpaka lero malowo amatchedwa Perezi Uza.

9 Tsiku limenelo Davide anachita mantha ndi Yehova ndipo anati, "Kodi Bokosi la Yehova lingafike bwanji kwathu?" 10 Iye sanafunenso kubwera
ndi Bokosi la Yehova kawo ku mzinda wake wa Davide. M'malo mwake anapita nalo ku nyumba ya Obedi-Edomu Mgiti. 11 Bokosi la Yehova
linakhala m'nyumba ya Obedi-Edomu Mgiti kwa miyezi itatu, ndipo Yehova anamudalitsa kwambiri iyeyo ndi banja lake lonse.

12 Tsono Mfumu Davide anawuzidwa kuti, "Yehova wadalitsa nyumba ya Obedi-Edomu ndi zonse zimene ali nazo, chifukwa cha Bokosi la Mulungu." Choncho Davide anapita kukatenga Bokosi la Mulungu ku nyumba ya Obedi-Edomu ndi kupita nalo ku mzinda wa Davide akukondwera kwambiri. 13 Anthu amene ananyamula Bokosi la Yehova
ankati akayenda mapazi asanu ndi limodzi, iye ankapereka nsembe ng'ombe yayimuna ndi mwana wang'ombe wonenepa. 14 Davide ankavina
ndi mphamvu zake zonse pamaso pa Yehova atavala efodi ya nsalu yofewa yosalala, 15 pamene iyeyo pamodzi ndi Aisraeli onse ankabwera ndi Bokosi
la Yehova, akufuwula ndi kuyimba malipenga.

16 Bokosi la Yehova likulowa mu Mzinda wa Davide, Mikala mwana wamkazi wa Sauli ankaona ali pa zenera. Ndipo ataona Mfumu Davide ikulumpha ndi kuvina pamaso pa Yehova, ankamunyogodola mu mtima mwake.

17 Iwo anabwera nalo Bokosi la Yehova ndipo analiyika pamalo pake m'kati mwa tenti imene Davide anayimika ndipo Davideyo anapereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano pamaso pa Yehova.
18 Atatsiriza kupereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano, iye anadalitsa anthu m'dzina la Yehova Wamphamvuzonse. 19 Kenaka iye
anagawira Aisraeli onsewo, aamuna ndi aakazi, aliyense buledi mmodzi, nthuli yanyama, ndiponso keke yamphesa zowuma. Ndipo anthu onse anachokapo, napita aliyense ku nyumba kwake.

20 Davide atabwerera ku nyumba kwake kukadalitsa banja lake, Mikala mwana wamkazi wa Sauli anatuluka kudzakumana naye ndipo anati, "Kodi mfumu ya Israeli ingatero kudzilemekeza kwake lero, kudzithyolathyola pamaso pa akapolo aakazi, antchito ake ngati munthu wamba."

21 Davide anamuyankha Mikala kuti, "Ndachita zimenezi molemekeza Yehova, amene anandisankha ine kupambana abambo ako, kapenanso kupambana banja la abambo ako. Ndipo anandisankha kuti ndikhale wolamulira Aisraeli, anthu a Yehova. N'chifukwa chake ndidzasangalalabe pamaso pa Yehova. 22 Ineyo ndidzadzinyoza kuposa apa, ndipo
ndidzakhala wonyozeka m'maso mwako. Koma pakati pa akapolo aakazi awa amene umanena za iwo, ndidzalemekezedwa."

23 Ndipo Mikala mwana wa Sauli sanakhalenso ndi mwana mpaka anamwalira.

# 7

*Lonjezo la Mulungu kwa Davide*

1 Mfumu itakhazikika m'nyumba yake yaufumu, Yehova atayipatsa
mpumulo kwa adani ake onse woyizungulira, 2 mfumuyo inawuza
mneneri Natani kuti, "Ine pano ndikukhala m'nyumba yomanga ndi
mitengo ya mkungudza, pomwe Bokosi la Mulungu lili mu tenti."

3 Natani anayankha mfumu kuti, "Chitani chilichonse chimene chili mu
mtima mwanu chifukwa Yehova ali nanu."

4 Usiku umenewo mawu a Yehova anafika kwa Natani ndipo anati,

5 "Pita kamuwuze mtumiki wanga Davide kuti, 'Yehova akunena
kuti: kodi ndiwe amene udzandimangira Ine nyumba yokhalamo?
6 Ine sindinakhalepo m'nyumba kuyambira tsiku limene ndinatulutsa
Aisraeli m'dziko la Igupto mpaka lero lino. Ndakhala ndikuyenda uku
ndi uku ndipo mokhala mwanga munali mu tenti. 7 Konse ndakhala
ndikuyenda ndi Aisraeli onse, kodi ndinanenapo kwa wina aliyense
atsogoleri awo, amene ndinamulamula kuweta anthu anga Aisraeli
kuti, n'chifukwa chiyani simunandimangire nyumba ya mitengo ya
mkungudza?' "

8 "Ndipo tsopano umuwuze mtumiki wanga Davide kuti, 'Yehova
Wamphamvuzonse akuti: Ine ndinakutenga ku busa ukuweta nkhosa
kuti ukhale mtsogoleri wa anthu anga Aisraeli. 9 Ineyo ndinali nawe
kulikonse kumene unkapita, ndipo ndachotsa adani ako onse pamaso
pako. Tsopano ndidzakuza dzina lako kuti likhale m'gulu la mayina
a anthu otchuka kwambiri pa dziko lapansi. 10 Ndipo ndidzawapatsa
malo anthu anga Aisraeli ndipo ndidzawadzala pamalo awoawo kuti
asadzavutitsidwenso. Anthu oyipa sadzawazunzanso monga ankachi-
tira poyamba paja, 11 monga akhala akuchitira kuchokera nthawi imene
ndinasankha atsogoleri a anthu anga Aisraeli. Ine ndidzakupatsaninso
mpumulo kwa adani anu onse.

" 'Yehova akulengeza kwa iwe kuti Iye mwini adzakhazikitsa banja
lako: 12 Masiku ako akadzatha ndipo ukadzakapuma ndi makolo
ako, Ine ndidzawutsa mphukira yako imene idzalowa m'malo mwako,
imene idzachokera m'thupi mwako, ndipo ndidzakhazikitsa ufumu
wake. 13 Iye ndiye amene adzamangire nyumba Dzina langa, ndipo Ine
ndidzakhazikitsa ufumu wake kwamuyaya. 14 Ine ndidzakhala abambo
ake, ndipo iye adzakhala mwana wanga. Akadzachita choyipa, Ineyo
ndidzamulanga ndi ndodo ndi zikwapu za anthu. 15 Koma sindidzasiya
kumukonda, monga ndinachitira ndi Sauli, amene ndinamuchotsa iwe
usanakhale mfumu. 16 Nyumba yako ndi ufumu wako zidzakhala
zamuyaya pamaso panga. Mpando wako waufumu udzakhazikika
kwamuyaya!' "

17 Natani anafotokozera Davide mawu onse avumbulutso limene ana-
landira.

*Pemphero la Davide*

18 Choncho Davide analowa mu tenti nakhala pamaso pa Yehova, ndipo
anati:

"Inu Yehova Wamphamvuzonse, ine ndine yani, ndipo banja langa
n'chiyani kuti mundifikitse pamene ndafikapa?" 19 Ndipo kukhala ngati
izi ndi zosakwanira pamaso panu, Inu Ambuye Wamphamvuzonse,
mwayankhula zatsogolo la banja la mtumiki wanu. Kodi umu ndi
mmene mumachitira ndi munthu, Inu Ambuye Wamphamvuzonse?

[20] Kodi Davide anenenso chiyani kwa Inu? Pakuti Inu Am-
buye Wamphamvuzonse mukumudziwa mtumiki wanu. [21] Chifukwa
cha mawu anu komanso mwa chifuniro chanu, mwachita chinthu
chachikulu ichi ndipo mwachiwulula kwa mtumiki wanu.

[22] Inu ndinu wamkulu, Yehova Wamphamvuzonse! Palibe wina
wofanana nanu, ndipo palibe Mulungu wina koma Inu nokha, monga
tamvera ndi makutu athu. [23] Ndipo ndi ndani wofanana ndi anthu
anu Aisraeli, mtundu wokhawo pa dziko lapansi umene Mulungu wake
anapita kukawuwombola monga anthu akeake ndi kukadzitchukitsa
yekha pochita zinthu zodabwitsa zazikulu, pothamangitsa mitundu ina
ndi milungu yawo pamaso pa anthu ake, amene Inu munawawombola
ku Igupto? [24] Inu mwawapanga anthu anu Aisraeli kukhala anuanu
kwamuyaya, ndipo Inu, Inu Yehova ndinu Mulungu wawo.

[25] "Ndipo tsopano Yehova Mulungu, sungani kwamuyaya lonjezo
limene mwachita ndi mtumiki wanu ndi banja lake. Chitani monga
mwalonjezera, [26] kotero dzina lanu lidzakhala lotchuka mpaka muyaya.
Ndipo anthu adzanena kuti, 'Yehova Wamphamvuzonse ndi Mulungu
wa Israeli!' Ndipo banja la mtumiki wanu Davide lidzakhazikika
pamaso panu.

[27] "Inu Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli, mwaululira
mtumiki wanu ponena kuti, 'Ine ndidzakumangira iwe nyumba!'
N'chifukwa chake ine mtumiki wanu ndalimba mtima kupemphera
motere. [28] Inu Ambuye Wamphamvuzonse, ndinu Mulungu! Mawu
anu ndi odalirika, ndipo mwalonjeza zinthu zabwinozi kwa mtumiki
wanu. [29] Ndipo tsopano chikukomereni kudalitsa banja la mtumiki
wanu, kuti likhale mpaka muyaya pamaso panu. Pakuti Inu, Yehova
Wamphamvuzonse, mwayankhula, ndipo ndi m'dalitso wanu banja la
mtumiki wanu lidzakhala lodalitsika mpaka muyaya."

# 8

## *Kupambana kwa Davide pa Nkhondo*

[1] Patapita nthawi, Davide anagonjetsa Afilisti ndi kuwapambana ndipo
analanda Metegi Ama kuchoka m'manja mwa Afilistiwo.

[2] Davide anagonjetsanso Amowabu. Iye anawalamula kuti agone pansi
m'mizere itatu pa gulu lililonse ndipo anawayeza ndi chingwe. Pa gulu
lililonse ankapha anthu amene anali pa mizere iwiri yoyamba, kusiyapo
mzere wachitatu. Kotero Amowabu anakhala pansi pa ulamuliro wa
Davide ndipo ankapereka msonkho.

[3] Komanso Davide anagonjetsa Hadadezeri mwana wa Rehobu, mfumu
ya Zoba, pamene anapita kukakhazikitsa ulamuliro wake m'mbali mwa
mtsinje wa Yufurate. [4] Davide analanda magaleta 1,000, anthu 7,000
okwera magaleta pamodzi ndi asilikali oyenda pansi 20,000. Iye anadula
mitsempha ya akavalo onse okoka magaleta, koma anasiyapo akavalo 100
okha.

[5] Aramu wa ku Damasiko atabwera kudzathandiza Hadadezeri mfumu
ya Zoba, Davide anakantha asilikali 22,000. [6] Iye anakhazikitsa maboma
mu ufumu wa Aramu wa ku Damasiko, ndipo Aaramu anakhala pansi
pa ulamuliro wake ndipo ankapereka msonkho. Yehova ankamupatsa
chipambano Davide kulikonse kumene ankapita.

7 Davide anatenga zishango zagolide za akuluakulu ankhondo a
Hadadezeri ndi kubwera nazo ku Yerusalemu. 8 Mfumu Davide inatenga
mkuwa wambiri kuchokera ku Beta ndi Berotai, mizinda ya Hadadezeri.

9 Tou, mfumu ya Hamati atamva kuti Davide wagonjetsa gulu lonse
lankhondo la Hadadezeri, 10 anatumiza mwana wake Yoramu kwa mfumu
Davide kukamulonjera ndi kukamuyamikira chifukwa cha kupambana
kwake pa nkhondo yake ndi Hadadezeriyo, amene analinso pa nkhondo
ndi Tou. Yoramu anabweretsa ziwiya zasiliva, zagolide ndi zamkuwa.

11 Mfumu Davide inapereka zinthu zimenezi kwa Yehova, monga
anachitira ndi siliva ndi golide zochokera ku mayiko onse amene anawag-
onjetsa: 12 Edomu ndi Mowabu, Aamoni ndi Afilisti, ndi Aamaleki. Iye
anaperekanso zolanda ku nkhondo zochokera kwa Hadadezeri mwana wa
Rehobu, mfumu ya Zoba.

13 Ndipo Davide anatchuka atabwera kokakantha Aedomu 18,000 mu
Chigwa cha Mchere.

14 Iye anayika maboma m'dera lonse la Edomu, ndipo Aedomu onse
anakhala pansi pa Davide. Yehova ankapambanitsa Davide kulikonse
kumene ankapita.

### *Akuluakulu a Davide*

15 Davide analamulira dziko lonse la Israeli ndipo ankachita zonse
mwachilungamo ndi molondola pamaso pa anthu ake onse. 16 Yowabu
mwana wa Zeruya anali mkulu wa ankhondo; Yehosafati mwana wa
Ahiludi anali mlembi wa zochitika. 17 Zadoki mwana wa Ahitubi ndi
Ahimeleki mwana wa Abiatara anali ansembe; Seraya anali mlembi;
18 Benaya mwana wa Yehoyada anali mtsogoleri wa Akereti ndi Apeleti;
ndipo ana a Davide anali ansembe.

# 9

### *Davide ndi Mefiboseti*

1 Davide anafunsa kuti, "Kodi alipo amene watsala m'banja la Sauli kuti
ndimuchitire chifundo chifukwa cha Yonatani?"

2 Tsono panali mtumiki wina wa banja la Sauli wotchedwa Ziba. Iwo
anamuyitana kuti aonekere pamaso pa Davide, ndipo mfumu inamufunsa
kuti, "Kodi ndiwe Ziba?"

Iyeyo anayankha kuti, "Ine mtumiki wanu."

3 Mfumu inafunsa kuti, "Kodi palibe amene watsala wa banja la Sauli
amene ndingamuchitire chifundo cha Mulungu?"

Ziba anayankha mfumu kuti, "Alipo mwana wa Yonatani, koma ndi
wolumala mapazi ake onse."

4 Mfumu inafunsa kuti, "Ali kuti?"

Ziba anayankha kuti, "Iye ali ku nyumba ya Makiri mwana wa Amieli
ku Lodebara."

5 Kotero mfumu inamubweretsa kuchokera ku Lodebara, ku nyumba ya
Makiri mwana wa Amieli.

6 Mefiboseti mwana wa Yonatani, mwana wa Sauli atafika kwa Davide,
anawerama pansi kupereka ulemu kwa iye.

Davide anati, "Mefiboseti!"

Iye anayankha kuti, "Ine mtumiki wanu."

7 Davide anati kwa iye, "Usachite mantha, pakuti ndidzakuchitira ndithu
chifundo chifukwa cha abambo ako Yonatani. Ine ndidzakubwezera iwe

dziko lonse limene linali la agogo ako Sauli, ndipo iweyo udzadya ndi ine
nthawi zonse.”
8 Mefiboseti anawerama pansi ndipo anati, “Mtumiki wanu ndine yani
kuti musamale galu wakufa ngati ine?”
9 Kenaka Davide anayitanitsa Ziba, mtumiki wa Sauli, ndipo anati, “Ine
ndapereka kwa chidzukulu cha mbuye wako chilichonse chimene chinali
cha Sauli ndi banja lake. 10 Iwe ndi ana ndi antchito anu muzimulimira
m’dziko lake ndipo muzibweretsa zokololazo kuti chidzukulu cha mbuye
wako chikhale ndi chakudya. Ndipo Mefiboseti, chidzukulu cha mbuye
wako adzadya ndi ine nthawi zonse.” (Tsono Ziba anali ndi ana aamuna
khumi ndi asanu ndi antchito makumi awiri).
11 Ndipo Ziba anati kwa mfumu, “Mtumiki wanu adzachita chilichonse
chimene mbuye wanga mfumu mudzalamulire wantchito wanu kuti
achite.” Kotero Mefiboseti ankadya ndi Davide monga mmodzi wa ana
a mfumu.
12 Mefiboseti anali ndi mwana wamng’ono wamwamuna wotchedwa
Mika, ndipo onse a banja la Ziba anali antchito a Mefiboseti. 13 Ndipo
Mefiboseti anakhala mu Yerusalemu chifukwa nthawi zonse amadya ndi
mfumu. Iye anali wolumala mapazi ake onse.

# 10

*Davide agonjetsa Aamoni*

1 Patapita nthawi, mfumu ya Aamoni inamwalira, ndipo mwana wake
Hanuni analowa ufumu m’malo mwake. 2 Davide anaganiza kuti, “Ine
ndidzachitira chifundo Hanuni mwana wa Nahasi chifukwa abambo
ake anandichitira zabwino.” Choncho Davide anatumiza anthu kuti
akamupepesere kwa Hanuni chifukwa cha imfa ya abambo ake.
Anthu amene Davide anawatuma atafika kwa Hanuni m’dziko la
Aamoni, 3 atsogoleri a ankhondo a Aamoni anawuza Hanuni mbuye wawo
kuti, “Kodi mukuganiza kuti Davide akupereka ulemu kwa abambo anu
potumiza anthuwa kwa inu kudzapepesa? Kodi Davide sanawatumize
anthuwa kuti adzaone mzinda wanu ndi kuchita ukazitape ndi cholinga
chofuna kuwulanda?” 4 Choncho Hanuni anagwira anthu amene Davide
anawatuma aja ndipo anameta munthu aliyense mbali imodzi ya ndevu
zake, ndi kudula zovala zake pakati m’chiwuno mpaka matako kuonekera,
ndipo anawabweza kwawo.
5 Atamufotokozera Davide zimenezi, iye anatuma amithenga kukaku-
mana ndi anthuwo chifukwa anali ndi manyazi kwambiri. Mfumu inati,
“Mukhale ku Yeriko mpaka ndevu zanu zitakula, ndipo kenaka mubwere
kuno.”
6 Aamoni atazindikira kuti amukwiyitsa kwambiri Davide, anakapeza
ankhondo oyenda pansi aganyu okwanira 20,000 kuchokera ku Asiriya wa
ku Beti Rehobu ndi Aramu-Zoba, komanso ankhondo 1,000 kwa mfumu
Maaka ndiponso ankhondo 22,000 ochokera ku Tobu.
7 Davide atamva zimenezi, anatumiza Yowabu ndi gulu lonse la
ankhondo amphamvu. 8 Aamoni anatuluka ndi kukhala m’mizere ya
nkhondo pa chipata cha mzinda wawo, pamene Aaramu a ku Aramu-Zoba
ndi Rehobu ndi ankhondo a ku Tobu ndi Maaka anali kwa wokha ku malo
wopanda mitengo.
9 Yowabu ataona kuti kunali mizere ya ankhondo kutsogolo kwake ndi
kumbuyo kwake, iye anasankha ena mwa ankhondo a Israeli odziwa

kuchita bwino nkhondo ndipo anawayika kuti amenyane ndi Aaramu.
10 Iye anayika ankhondo ena otsalawo m'manja mwa Abisai m'bale wake
ndipo anawayika kuti amenyane ndi Aamoni. 11 Yowabu anati, "Ngati
Aaramu andipose mphamvu, iwe ubwere udzandipulumutse. Koma
ngati Aamoni akupose mphamvu, ine ndidzabwera kudzakupulumutsa.
12 Limba mtima ndipo timenyane nawo mopanda mantha chifukwa cha
anthu athu ndi mizinda ya Mulungu wathu. Yehova achite chomukomera
pamaso pake."

13 Choncho Yowabu ndi ankhondo amene anali naye anapita kuka-
menyana ndi Aaramu, ndipo iwo anathawa pamaso pake. 14 Aamoni
atazindikira kuti Aaramu akuthawa, iwo anathawanso pamaso pa Abisai
ndi kulowa mu mzinda. Nkhondo itatha, Yowabu anabwerera ku
Yerusalemu.

15 Aaramu ataona kuti agonjetsedwa ndi Aisraeli, anasonkhananso.
16 Hadadezeri anatumiza amithenga kukayitana Aaramu amene anali ku
tsidya la Mtsinje, iwo anapita ku Helamu motsogozedwa ndi Sobaki mkulu
wa ankhondo a Hadadezeri.

17 Davide atawuzidwa zimenezi, iye anasonkhanitsa Aisraeli onse
ndi kuwoloka Yorodani ndipo anapita ku Helamu. Aaramu anayima
m'mizere yawo yankhondo kukakumana ndi Davide ndipo anamenyana
naye. 18 Koma iwo anathawa pamaso pa Aisraeli, ndipo Davide anapha
anthu okwera pa magaleta 700 ndi ankhondo oyenda pansi 40,000.
Davide anaphanso Sobaki mtsogoleri wawo wankhondo ndipo anafera
pomwepo. 19 Mafumu onse amene anali pansi pa Hadadezeri ataona
kuti agonjetsedwa ndi Aisraeli, iwo anachita mtendere ndi Aisraeli ndipo
anakhala pansi pawo.

Motero Aaramu anaopa kuthandizanso Aamoni.

# 11

### *Davide ndi Batiseba*

1 Nthawi ya mphukira, nthawi imene mafumu amapita ku nkhondo,
Davide anatumiza Yowabu ndi ankhondo a mfumu pamodzi ndi gulu lonse
lankhondo la Aisraeli. Iwo anawononga Aamoni ndi kuzungulira mzinda
wa Raba. Koma Davide anatsala ku Yerusalemu.

2 Tsiku lina cha kumadzulo Davide anadzuka pa bedi lake ndipo
ankayenda pamwamba pa nyumba yake. Ali pa dengapo anaona mkazi
akusamba. Mkaziyo anali wokongola kwambiri. 3 Ndipo Davide anatuma
munthu wina kuti akafufuze za iye. Munthuyo anati, "Kodi uyu si
Batiseba, mwana wa Eliamu, mkazi wa Uriya Mhiti?" 4 Ndipo Davide
anatumiza amithenga kwa iye kukamuyitana. Batiseba anabwera kwa
Davide ndipo anagona naye. (N'kuti mkaziyu atayeretsedwa ku masiku
ake osamba). Kenaka anabwerera ku nyumba yake. 5 Mkaziyo anakhala
woyembekezera ndipo anatumiza mawu kwa Davide kunena kuti, "Ine
ndine woyembekezera."

6 Ndipo Davide anatumiza mawu awa kwa Yowabu: "Nditumizire Uriya
Mhiti." Ndipo Yowabu anamutumiza kwa Davide. 7 Uriya atafika kwa
Davide, Davide anamufunsa za momwe analili Yowabu, za asilikali ndi
momwe nkhondo inkayendera. 8 Kenaka Davide anati kwa Uriya, "Pita
ku nyumba yako ukapumule." Choncho Uriya anachoka ku nyumba
yaufumu, ndipo mfumuyo inatumiza mphatso kwa Uriya. 9 Koma Uriya

anagona pa chipata cha nyumba yaufumu pamodzi ndi antchito onse a
mbuye wake ndipo sanapite ku nyumba yake.
[10] Davide atawuzidwa kuti, "Uriya sanapite ku nyumba yake." Iye
anafunsa kuti, "Kodi iwe sunachokera kutali? N'chifukwa chiyani
sunapite ku nyumba yako?"
[11] Uriya anayankha Davide kuti, "Bokosi la Chipangano ndi Israeli
ndiponso Yuda akukhala m'matenti, ndipo mbuye wanga Yowabu ndi
ankhondo anu mbuye wanga amanga misasa pa mtetete. Ine ndingapite
bwanji ku nyumba yanga kukadya ndi kumwa ndiponso kugona ndi mkazi
wanga? Pali inu wamoyo, ine sindidzachita chinthu chimenechi."
[12] Ndipo Davide anati kwa iye, "Ukhale konkuno tsiku lina limodzi, ndipo
mawa ndikulola kuti upite." Kotero Uriya anakhala mu Yerusalemu tsiku
limenelo ndi tsiku linalo. [13] Davide anayitana Uriya nadya ndi kumwa
naye, ndipo Davide anamuledzeretsa. Koma madzulo Uriya anapita
kukagona pa mphasa pamodzi ndi antchito a mbuye wake. Iye sanapite
ku nyumba yake.
[14] Mmawa Davide analemba kalata kwa Yowabu ndipo anayitumiza
ndi Uriya. [15] M'kalatayo analembamo kuti, "Uriya mumuyike patsogolo
penipeni, pamene pali nkhondo yoopsa. Ndipo mumusiye yekha kuti
akanthidwe ndi kufa."
[16] Kotero Yowabu atawuzinga mzindawo, anamuyika Uriya pamalo
pamene amadziwa kuti pali asilikali amphamvu. [17] Ankhondo a mu
mzindawo atabwera kudzamenyana ndi Yowabu, anthu ena a gulu la
ankhondo la Davide anaphedwa ndipo Uriya Mhiti uja anaphedwanso.
[18] Yowabu anatumiza wamthenga kwa Davide kukafotokoza mwatsa-
tanetsatane za nkhondoyo. [19] Iye anamulangiza wa mthengayo kuti,
"Pamene ukatsiriza kufotokozera mfumu za ku nkhondozi, [20] mfumu
ikapsa mtima, ndipo akakakakufunsa kuti, 'N'chifukwa chiyani munapita
pafupi ndi mzindawo kukamenya nkhondo? Inu simunadziwe kuti atha
kukuponyerani mivi kuchokera pa khoma? [21] Kodi anapha Abimeleki
mwana wa Yerubeseti ndani? Kodi mkazi sanamuponyere mphero
kuchokera pa khoma? Kotero kuti anakafera ku Tebezi. N'chifukwa
chiyani munafika pafupi ndi khoma?' Ngati iye akafunsa zimenezi, iwe
ukanene kwa iye kuti, 'Mtumiki wanunso Uriya Mhiti wafa.' "
[22] Mthengayo ananyamuka, ndipo atafika anamuwuza Davide zonse
zimene Yowabu anamutuma kuti akanene. [23] Mthengayo anati kwa
Davide, "Anthuwo anatiposa mphamvu ndipo anabwera kudzalimbana
nafe poyera, koma ife tinawabwezera ku chipata cha mzindawo. [24] Ndipo
anthu oponya mivi anatiponyera kuchokera pa khoma, anthu ena a
mfumu afa. Kuwonjezera apo, mtumiki wanu Uriya Mhiti wafanso."
[25] Davide anamuwuza mthengayo kuti, "Ukanene izi kwa Yowabu:
'Zimenezi zisakukhumudwitse; lupanga limapha wina nthawi zinanso
wina. Limbikitsa nkhondo pa mzindawo ndipo uwuwononge!' Ukanene
zimenezi pomulimbikitsa Yowabu."
[26] Mkazi wa Uriya atamva kuti mwamuna wake wafa, analira maliro.
[27] Nthawi yolira maliro itatha, Davide anamubweretsa ku nyumba yake,
ndipo anakhala mkazi wake nabala mwana wamwamuna. Koma Yehova
sanakondwe ndi zimene Davide anachitazo.

# 12

*Natani Adzudzula Davide*

1 Tsono Yehova anatumiza Natani kwa Davide. Atafika kwa Davide anati,
“Panali anthu awiri m’mizinda ina, wina wolemera ndi wina wosauka.
2 Munthu wolemerayo anali ndi nkhosa ndi ng’ombe zambiri, 3 koma
wosaukayo analibe chilichonse kupatula kankhosa kamodzi kakakazi
kamene anakagula. Iye anakasunga ndipo kanakula naye pamodzi ndi
ana ake. Kamadya chakudya chake, kamamwera chikho chake ndipo
kamagona m’manja mwake. Kanali ngati mwana wamkazi kwa iyeyo.
4 “Ndipo mlendo anafika kwa munthu wolemera uja, koma munthu
wolemerayo sanafune kutenga imodzi mwa nkhosa kapena ng’ombe zake
kuti akonzere chakudya mlendo amene anafika kwa iye. M’malo mwake
anatenga mwana wankhosa wamkazi wa munthu wosauka uja nakonzera
chakudya mlendo uja amene anabwera kwa iye.”
5 Davide anapsa mtima kwambiri chifukwa cha munthuyo ndipo anati
kwa Natani, “Pali Yehova, munthu amene anachita zimenezi ayenera
kufa basi! 6 Iye ayenera kulipira mwana wankhosa wamkaziyo kanayi,
chifukwa anachita chinthu chimenechi ndipo analibe chifundo.”
7 Kenaka Natani anati kwa Davide, “Munthuyo ndinu! Yehova,
Mulungu wa Israeli akuti, ‘Ine ndinakudzoza kukhala mfumu ya Israeli,
ndipo ndinakupulumutsa m’dzanja la Sauli. 8 Ndinakupatsanso banja
la mbuye wako ndiponso akazi a mbuye wako m’manja mwako. Ine
ndinakupatsanso banja la Israeli ndi Yuda. Ndipo ngati zinthu zonse
izi zinali zochepa, Ine ndikanakupatsa zambiri. 9 N’chifukwa chiyani
unanyoza mawu a Yehova pochita chimene chili choyipa pamaso pake?
Iwe unakantha Uriya Mhiti ndi lupanga ndipo unatenga mkazi wake
kukhala wako. Uriyayo unamupha ndi lupanga la Aamoni. 10 Ndipo
tsopano lupanga silidzachoka pa nyumba yako, chifukwa unandinyoza ine
ndi kutenga mkazi wa Uriya Mhiti kukhala wako.’
11 “Yehova akuti, ‘Ine ndidzabweretsa tsoka pa iwe lochokera m’banja
lako. Ndidzatenga akazi ako iwe ukuona ndi kuwapereka kwa wina amene
ali pafupi nawe, ndipo iye adzagona ndi akazi ako masanasana Aisraeli
onse akuona. 12 Iwe unachita zimenezi mwamseri koma Ine ndidzachita
izi masanasana Aisraeli onse akuona.’ ”
13 Kenaka Davide anati kwa Natani, “Ine ndachimwira Yehova.”

Natani anayankha kuti, “Yehova wachotsa tchimo lanu. Simufa ayi.
14 Komabe, popeza pochita zimenezi mwachititsa kuti adani a Yehova
amunyoze, mwana amene akubalireniyo adzafa.”
15 Natani atapita kwawo, Yehova anakantha mwana amene mkazi wa
Uriya anabereka ndipo anayamba kudwala. 16 Davide anapempherera
mwanayo kwa Mulungu. Iye anasala chakudya ndipo analowa m’nyumba
mwake nagona pansi usiku wonse. 17 Akuluakulu a banja lake anayima
pambali pake kuti amudzutse, koma iye anakana, ndipo sanadye chakudya
chilichonse pamodzi ndi iwo.
18 Mwana anamwalira pa tsiku lachisanu ndi chiwiri. Antchito a
Davide anaopa kumuwuza kuti mwanayo wamwalira, popeza ankaganiza
kuti, “Pamene mwanayu anali ndi moyo, ife tinayankhula Davide koma
sanatimvere. Nanga tingamuwuze bwanji kuti mwana wamwalira?
Mwina atha kudzipweteka.”
19 Davide anaona kuti antchito ake amanong’onezana pakati pawo
ndipo anazindikira kuti mwanayo wamwalira. Iye anafunsa kuti, “Kodi
mwanayo wamwalira?”

Iwo anayankha kuti, “Inde wamwalira.”

20 Ndipo Davide anayimirira. Anakasamba nadzola mafuta ndi kusintha
zovala zake. Pambuyo pake anapita ku nyumba ya Yehova kukapembedza.
Kenaka anapita ku nyumba kwake ndipo atapempha chakudya anamu-
patsa nadya.
21 Antchito ake anamufunsa kuti, "Chifukwa chiyani mukuchita zinthu
motere? Pamene mwana anali ndi moyo, munkasala chakudya ndi kulira,
koma tsopano pamene mwana wamwalira inu mukudzuka ndi kudya!"
22 Iye anayankha kuti, "Pamene mwana anali ndi moyo ine ndinkasala
zakudya ndi kulira. Ine ndinkaganiza kuti, 'Akudziwa ndani? Yehova atha
kundikomera mtima kuti mwanayo akhale ndi moyo.' 23 Koma tsopano
wamwalira ndisaliranji chakudya? Kodi ndingathe kumubwezanso? Ine
ndidzapita kumene kuli iyeko, koma iye sadzabwerera kwa ine."
24 Ndipo Davide anatonthoza mkazi wake Batiseba, napita kwa iye ndi
kugona naye. Iye anabereka mwana wamwamuna, ndipo anamutcha
dzina lake Solomoni. Yehova ankamukonda iye. 25 Ndipo chifukwa chakuti
Yehova ankamukonda iyeyo, Yehovayo anatumiza mawu kwa mneneri
Natani kuti akamutchule Yedidiya.
26 Pa nthawi imeneyi Yowabu anamenyana ndi Raba ku Amoni ndipo
analanda nsanja yaufumu. 27 Ndipo Yowabu anatumiza amithenga kwa
Davide kukanena kuti, "Ine ndamenyana ndi Raba ndipo ndatenga zitsime
zake za madzi. 28 Ndipo tsopano sonkhanitsani asilikali onse ndipo
muzungulire mzindawo ndi kuwulanda."
29 Kotero Davide anasonkhanitsa ankhondo onse ndipo anapita ku Raba
kukawuthira nkhondo ndi kuwulanda. 30 Davide anachotsa chipewa
chaufumu pamutu pa mfumu yawo ndipo Davide anavala chipewacho.
Chipewacho chinkalemera makilogalamu asanu agolide, ndiponso chinali
ndi miyala yokongola. Iye anatenga katundu wambiri kuchokera mu
mzindawo, 31 ndipo anatulutsa anthu amene anali m'menemo, nawayika
kuti azigwira ntchito ya macheka, yosula makasu ndi nkhwangwa,
ndiponso yowomba njerwa. Davide anachita izi ndi mizinda yonse ya
Aamoni. Kenaka iye pamodzi ndi gulu lake lonse lankhondo anabwerera
ku Yerusalemu.

# 13

*Amnoni ndi Tamara*

1 Patapita nthawi, Amnoni mwana wa Davide anakonda Tamara, mlongo
wa Abisalomu, mwana wa Davide, amene anali wokongola.
2 Amnoni sankagona tulo mpaka anadwala chifukwa cha Tamara
mlongo wakeyo, pakuti iye anali asanagonepo ndi mwamuna ndipo
zimaoneka kuti zinali zosatheka kuti achite chilichonse kwa iye.
3 Koma Amnoni anali ndi mnzake dzina lake Yehonadabu mwana
wamwamuna wa Simea, m'bale wake wa Davide. Yonadabu anali munthu
wochenjera kwambiri. 4 Iye anafunsa Amnoni, "N'chifukwa chiyani iwe
mwana wa mfumu, umaoneka wowonda mmawa uliwonse? Bwanji
wosandiwuza?"
Amnoni anamuyankha kuti, "Ine ndamukonda Tamara, mlongo wa
m'bale wanga Abisalomu."
5 Yehonadabu anati, "Pita ukagone ndipo unamizire kudwala. Abambo
ako akabwera kudzakuona, udzati kwa iwo, Ine ndikufuna mlongo
wanga Tamara abwere kuti adzandikonzere chakudya kuti ndidye.
Adzandikonzere chakudyacho ine ndikumuona ndi kudya chili m'manja
mwake."

6 Kotero Amnoni anagona nakhala ngati akudwala. Mfumu itab-
wera kudzamuona, Amnoni anati kwa iyo, “Ine ndikufuna mlongo
wanga Tamara kuti abwere adzandipangire buledi wapamwamba ineyo
ndikuona, kuti ndidye ali m’manja mwake.”
7 Davide anatumiza mawu kwa Tamara ku nyumba yaufumu kuti, “Pita
ku nyumba ya mlongo wako Amnoni ndipo ukamukonzere chakudya.”
8 Choncho Tamara anapitadi ku nyumba ya mlongo wake Amnoni
kumalo kumene ankagona. Anakanda ufa, nawumba buledi Amunoniyo
akuona ndipo anaphika bulediyo. 9 Kenaka iye anatenga chiwaya ndipo
anamupatsa bulediyo, koma iyeyo anakana.
Amnoni anati “Uza aliyense atuluke muno.” Ndipo aliyense anatuluka.
10 Kenaka Amnoni anati kwa Tamara, “Bweretsa chakudya kuno, ku
chipinda changa chogona kuti ndidye chili m’manja mwako.” Ndipo
Tamara anatenga buledi amene anapanga ndi kubwera naye kwa mlongo
wake ku chipinda chake. 11 Koma atabweretsa kwa iye kuti adye,
anamugwira ndipo anati, “Bwera ugone nane, iwe mlongo wanga.”
12 Tamara anati kwa iye, “Ayi mlongo wanga! Usandikakamize. Zotere
siziyenera kuchitika mu Israeli! Usachite chinthu choyipa chotere. 13 Kodi
ukuganiza bwanji za ine? Kodi manyazi anga ndidzawachotsa bwanji?
Ndipo nanga iweyo? Udzakhalatu monga mmodzi mwa zitsiru zoyipitsitsa
muno mu Israeli. Chonde kapemphe kwa mfumu. Sadzakuletsa kuti
undikwatire.” 14 Koma sanamvere zimene amanena Tamara ndipo popeza
anali wamphamvu kuposa Tamarayo, iye anamugwirira.
15 Atatero Amnoni anadana naye kwambiri. Iyeyo anamuda kuposa
momwe anamukondera. Amnoni anati, “Dzuka ndipo tuluka!”
16 Iye anayankha, “Ayi! Kundithamangitsa kukhala kulakwa kwakukulu
kuposa zimene wachita kale kwa ine.”
Koma anakana kumumvera. 17 Amnoni anayitana wantchito wake ndipo
anati, “Mutulutse mkazi uyu muno ndipo utseke chitseko akatuluka.”
18 Choncho wantchito wakeyo anamutulutsa ndipo anatseka chitseko atat-
uluka. Tamara anali atavala mkanjo wokongoletsedwa kwambiri, pakuti
ichi chinali chovala chimene ana aakazi a mfumu amene sanagonepo
ndi mwamuna amavala. 19 Tamara anatsira phulusa pamutu pake ndipo
anang’amba mkanjo wokongoletsedwa umene anavalawo. Iye anagwira
manja ake kumutu ndipo anachoka, akulira mokweza pamene amapita.
20 Mlongo wake Abisalomu anati, “Kodi Amnoni uja mlongo wako
wagona nawe? Khala chete mlongo wanga. Iye uja ndi mlongo wako
ndipo usazilabadire.” Choncho Tamara anakhala m’nyumba ya Abisalomu
mlongo wake ngati woferedwa.
21 Mfumu Davide itamva zimenezi, inakwiya kwambiri. 22 Abisalomu
sananene mawu aliwonse kwa Amnoni; abwino kapena oyipa. Iye ana-
muda Amunoniyo chifukwa anachititsa manyazi mlongo wake Tamara.

### *Abisalomu Apha Amnoni*

23 Patapita zaka ziwiri, pamene wometa nkhosa za Abisalomu anali ku
Baala-Hazori pafupi ndi malire a fuko la Efereimu, iye anayitana ana onse
aamuna a mfumu kuti apite kumeneko. 24 Abisalomu anapita kwa mfumu
ndipo anati, “Ometa nkhosa za mtumiki wanu anabwera. Chonde mfumu
ndi akuluakulu anu mubwere kudzakhala nane?”
25 Mfumu inayankha kuti, “Ayi mwana wanga, tisapite tonsefe. Tidza-
khala cholemetsa kwa iwe.” Ngakhale Abisalomu anayesetsa kuwumiriza
mfumuyo, inakana kupita. M’malo mwake inangomudalitsa Abisalomuyo.

26 Kenaka Abisalomu anati, “Ngati sizitero, chonde mulole m’bale wanga
Amnoni apite nane.”

Mfumu inamufunsa kuti, “Apite nawe chifukwa chiyani?” 27 Koma
Abisalomu anamuwumiriza, kotero analola kuti Amnoni pamodzi ndi ana
onse a mfumu apite naye.

28 Abisalomu analamula antchito ake kuti, “Tamverani! Amnoni
akakaledzera ndi vinyo ndipo ine ndikakanena kuti, ‘Mukantheni Am-
noni,’ pamenepo mukamuphe. Musakachite mantha. Kodi ine sindinaku-
lamuleni? Mukhale amphamvu ndipo mulimbe mtima.” 29 Kotero antchito
a Abisalomu anachita kwa Amnoni zimene Abisalomu anawalamula.
Kenaka ana onse a mfumu anayimirira ndipo anakwera pa abulu awo
nathawa.

30 Ali m’njira, Davide anamva mphekesera yakuti, “Abisalomu wakantha
ana onse a mfumu ndipo palibe ndi mmodzi yemwe amene watsala.”
31 Mfumu inayimirira, ning’amba zovala zake ndi kugona pa dothi.
Antchito ake onse anayimirira pomwepo atang’amba zovala zawo.

32 Koma Yehonadabu mwana wa Simea, m’bale wake wa Davide anati,
“Mbuye wanga mfumu musaganize kuti wapha ana onse a mfumu; wafa
ndi Amnoni yekha. Awa ndiwo akhala maganizo a Abisalomu kuyambira
tsiku limene Amnoni anagwirira mlongo wake Tamara. 33 Mbuye wanga
mfumu musavutike ndi maganizo ndi nkhani yoti ana onse a mfumu afa.
Wafa ndi Amnoni yekha.”

34 Nthawi imeneyi n’kuti Abisalomu atathawa.

Tsono munthu amene amalondera anayang’ana ndipo anaona anthu
ambiri pa msewu wa kumadzulo kwake, akubwera kutsetsereka phiri.
Mlondayo anapita kukawuza mfumu kuti, “Ndikuona anthu pa njira ya
Horonaimu, m’mbali mwa phiri.”

35 Yehonadabu anati kwa mfumu, “Taonani ana a mfumu afika.
Zachitika monga momwe mtumiki wanu ananenera.”

36 Pamene amatsiriza kuyankhula, ana a mfumu analowa, akulira
mofuwula. Mfumunso ndi antchito ake onse analira mokhudzidwa.

37 Abisalomu anathawa, napita kwa Talimai mwana wa Amihudi,
mfumu ya ku Gesuri. Koma mfumu Davide inalira mwana wake tsiku
ndi tsiku.

38 Abisalomu atathawa ndi kupita ku Gesuri, anakhala kumeneko zaka
zitatu. 39 Ndipo Davide anagwidwa ndi chifundo chofuna kumulondola
Abisalomu pakuti anali atatonthozedwa pa imfa ya Amnoni.

# 14

*Abisalomu Abwerera ku Yerusalemu*

1 Yowabu mwana wa Zeruya anadziwa kuti maganizo a mfumu ali pa
Abisalomu. 2 Kotero Yowabu anatuma munthu wina kupita ku Tekowa ndi
kukatengako mkazi wanzeru. Yowabu anati kwa mkaziyo, “Ukhale ngati
namfedwa. Uvale zovala zaumasiye ndipo usadzole mafuta ena aliwonse.
Ukhale ngati mkazi amene wakhala akulira masiku ambiri. 3 Kenaka upite
kwa mfumu ndipo ukayankhule mawu awa.” Ndipo Yowabu anamuwuza
mawu oti akanene.

4 Mkazi wochokera ku Tekowa uja atapita kwa mfumu anadzigwetsa
pansi, napereka ulemu kwa mfumu nati, “Thandizeni mfumu!”

5 Mfumu inamufunsa kuti, “Kodi chikukusautsa iwe n’chiyani?”

Iye anayankha kuti, “Ine ndine mkazi wamasiye, mwamuna wanga
anamwalira. 6 Ine wantchito wanu ndinali ndi ana aamuna awiri.
Iwo anayamba kumenyana m’munda, ndipo panalibe woti awaleretse.
Wina anakantha mnzakeyo mpaka kumupha. 7 Tsono banja lonse
landiwukira ine, wantchito wanu. Iwo akuti, ‘Utipatse mwana amene
anakantha m’bale wakeyo kuti timuphe chifukwa cha moyo wa m’bale
wake amene anaphedwayo. Ife tidzaphanso mlowam’malo.’ Anthuwo
adzapha mwana wanga amene wanditsalira, ndipo dzina la mwamuna
wanga silidzakumbukika pakuti sipadzakhalanso mwana pa banja lathu.”

8 Mfumu inati kwa mkaziyo, “Pitani ku nyumba kwanu ndipo ine
ndidzalamula m’malo mwanu.”

9 Koma mkazi wochokera ku Tekowayo anati kwa mfumu, “Mbuye
wanga mfumu, kulakwa kukhale pa ine ndi banja la abambo anga ndipo
mfumu ndi mpando wanu waufumu mukhale osalakwa.”

10 Mfumu inayankha kuti, “Ngati wina aliyense anene kanthu kwa iwe,
umubweretse kwa ine, ndipo sadzakuvutitsanso.”

11 Mkaziyo anati, “Mfumu ipemphe kwa Yehova Mulungu wake
kuti aletse wobwezera imfa asaphenso wina kuti mwana wanga
asawonongedwe.”

Mfumu inati, “Pali Yehova wamoyo ngakhale tsitsi limodzi la pamutu pa
mwana wako silidzathotholedwa.”

12 Kenaka mkaziyo anati, “Lolani kuti wantchito wanu ayankhule mawu
kwa inu mbuye wanga mfumu.”

Iye anayankha kuti, “Yankhula.”

13 Mkaziyo anati, “N’chiyani tsono chimene mwaganiza kuchitira
zimenezi anthu a Mulungu? Pamene mfumu yanena izi, kodi sikudzit-
sutsa yokha, pakuti mfumu sinayitanitse mwana amene anamupirikitsa?
14 Koma poti madzi akatayika sawoleka, ndiye tonsefe tiyenera kufa
ndithu. Koma Mulungu safuna kuti moyo wa munthu utayike kotero
anakonza njira yakuti wopirikitsidwayo asakhale wotayikiratu.

15 “Tsopano ine ndabwera kudzanena izi kwa inu mbuye wanga mfumu
chifukwa anthu andichititsa mantha. Mdzakazi wanu anaganiza kuti,
‘Ndikayankhula kwa mfumu, mwina adzachita zimene mdzakazi wake
adzamupempha. 16 Mwina mfumu idzavomereza kupulumutsa mdzakazi
wake m’dzanja la munthu amene akufuna kupha ine pamodzi ndi mwana
wanga kutichotsa pa cholowa chimene Mulungu anatipatsa.’

17 “Ndipo tsopano mtumiki wanu akuti, ‘Lolani mawu a mbuye wanga
mfumu abweretse mpumulo kwa ine, pakuti mbuye wanga mfumu ali
ngati mngelo wa Mulungu pozindikira chabwino ndi choyipa. Yehova
Mulungu wanu akhale nanu.’ ”

18 Kenaka mfumu inati kwa mkaziyo, “Usandibisire chilichonse
pondiyankha chimene ndidzakufunsa.”

Mkaziyo anati, “Mbuye wanga mfumu yankhulani.”

19 Mfumu inafunsa kuti, “Kodi zimenezi sukuchita motsogozedwa ndi
Yowabu?”

Mkaziyo anayankha kuti, “Pali inu wamoyo, mbuye wanga mfumu,
palibe munthu angakhotere kumanja kapena kumanzere pa chili-
chonse chimene mbuye wanga mfumu mwanena. Inde, ndi mtumiki
wanu Yowabu amene wandilangiza ine kuchita zimenezi ndipo ndi
amene anandipatsa mawu onsewa woti ine mtumiki wanu ndiyankhule.
20 Mtumiki wanu Yowabu anachita zimenezi kuti asinthe mmene zinthu

zilili lero. Mbuye wanga muli ndi nzeru ngati za mngelo wa Mulungu.
Mumadziwa zonse zimene zikuchitika m’dziko.”
21 Mfumu inati kwa Yowabu, “Chabwino, ine ndichita zimenezi. Pita
kamutenge Abisalomuyo.”
22 Yowabu anawerama pansi kupereka ulemu kwa mfumu. Yowabuyo
anati, “Lero mtumiki wanu wadziwa kuti wapeza chifundo pamaso panu,
mbuye wanga mfumu, chifukwa mwavomera pempho lakeli.”
23 Choncho Yowabu anapita ku Gesuri ndipo anamubweretsa Abisalomu
ku Yerusalemu. 24 Koma mfumu inati, “Iye apite ku nyumba yake;
asaone nkhope yanga.” Kotero Abisalomu anapita ku nyumba yake ndipo
sanakumane ndi mfumu.
25 M’dziko lonse la Israeli munalibe munthu amene anayamikidwa
chifukwa cha maonekedwe ake wokongola ngati Abisalomu. Kuyambira
kumutu mpaka ku mapazi ake, analibe chilema. 26 Nthawi ina iliyonse
akamameta tsitsi lake, ankameta pamene layamba kumulemera. Akatero
amaliyeza, ndipo limalemera makilogalamu awiri pa sikelo yaufumu.
27 Abisalomu anali ndi ana aamuna atatu ndi wamkazi mmodzi.
Mwana wamkazi dzina lake linali Tamara, ndipo anali mkazi wokongola
kwambiri.
28 Abisalomu anakhala zaka ziwiri mu Yerusalemu osaonekera kwa
mfumu. 29 Kenaka Abisalomu anatumiza mawu kwa Yowabu, kumutuma
kuti apite kwa mfumu, koma Yowabu anakana kubwera. Kotero anatu-
mizanso mawu kachiwiri, koma Yowabu anakananso. 30 Tsono Abisalomu
anati kwa antchito ake, “Taonani, munda wa Yowabu uli pafupi ndi wanga
ndipo muli barele m’menemo. Pitani mukawutenthe mundawo.” Ndipo
antchito a Abisalomu anawutentha mundawo.
31 Ndipo Yowabu anapita ku nyumba ya Abisalomu ndipo anati kwa iye,
“N’chifukwa chiyani antchito ako atentha munda wanga?”
32 Abisalomu anati kwa Yowabu, “Taona, ine ndinatumiza mawu kwa
iwe ndipo ndinati, ‘Bwera kuno kuti ndikutume kwa mfumu kuka-
funsa kuti, ‘N’chifukwa chiyani ine ndinabwera kuchokera ku Gesuri?
Zikanakhala bwino ndikanakhala komweko!’ Tsono pano ndikufuna
kuonana ndi mfumu, ndipo ngati ndili olakwa mfumuyo indiphe.’ ”
33 Choncho Yowabu anapita kwa mfumu ndipo anayiwuza zimenezi.
Ndipo mfumu inamuyitanitsa Abisalomu, ndipo analowa nawerama
kugunditsa nkhope yake pansi pamaso pa mfumu. Tsono mfumu
inapsompsona Abisalomu.

# 15

*Abisalomu Akonzekera Zowukira*

1 Patapita nthawi, Abisalomu anadzipezera galeta ndi akavalo pamodzi
ndi amuna makumi asanu amene amathamanga patsogolo pake. 2 Iye
amadzuka mmamawa ndi kuyima pa njira yopita ku chipata cha mzinda.
Munthu wina aliyense akakhala ndi zodandaula zopita nazo kwa mfumu
kuti akaweruze, Abisalomu amamuyitana iye ndi kumufunsa kuti, “Kodi
ukuchokera ku limodzi mwa mafuko a Israeli?” 3 Kenaka Abisalomu
amanena kwa iye kuti, “Taona, madandawulo ako ndi abwino ndi oyenera,
koma palibe woyimira mfumu woti akumvere.” 4 Ndipo Abisalomu ama-
wonjezera kunena kuti, “Ine ndikanangosankhidwa kukhala woweruza
m’dziko muno bwenzi munthu aliyense amene ali ndi madandawulo

kapena milandu akubwera kwa ine ndipo ndikanaonetsetsa kuti chilung-
amo chachitika.”
5 Ndipo nthawi zonse amati munthu akasendera pafupi ndi kumug-
wandira, Abisalomu amatambalitsa dzanja lake, kumuyimiritsa munthuyo
ndi kupsompsona. 6 Abisalomu amachitira izi Aisraeli onse amene
amabwera kwa mfumu kuti adzaweruzidwe ndipo Abisalomuyo anagwira
mtima anthu a mu Israeli.
7 Patapita zaka zinayi Abisalomu anati kwa mfumu, “Loleni ndipite
ku Hebroni kuti ndikakwaniritse lonjezo limene ndinachita kwa Yehova.
8 Pamene mtumiki wanu amakhala ku Gesuri ku Aramu, anachita lonjezo
ili: ‘Ngati Yehova adzandibweretsadi ku Yerusalemu, ndidzapembedza
Yehovayo mu Hebroni.’ ”
9 Mfumu inati kwa iye, “Pita mu mtendere” Kotero iye anapita ku
Hebroni.
10 Ndipo Abisalomu anatuma amithenga ake mwamseri kwa mafuko
onse a Israeli kukanena kuti, “Mukangomva kulira kwa malipenga
pamenepo munene kuti, ‘Abisalomu ndiye mfumu mu Hebroni.’ ” 11 Anthu
200 ochokera mu Yerusalemu anapita naye Abisalomu. Iwo anayitanidwa
monga alendo ndipo anapita osadziwa chilichonse pa nkhaniyi. 12 Pamene
Abisalomu amapereka nsembe, iye anayitanitsanso Ahitofele Mgiloni,
mlangizi wa Davide, wa ku Gilo, kotero kuwukiraku kunakula kwambiri,
ndipo anthu otsatira Abisalomu anapitirira kuchuluka.

### *Davide Athawa Abisalomu*

13 Munthu wina anabweretsa uthenga ndi kudzamuwuza Davide kuti,
“Mitima ya Aisraeli onse ili pa Abisalomu.”
14 Ndipo Davide anati kwa akuluakulu ake amene anali mu Yerusalemu.
“Bwerani! Tiyeni tithawe, mwina palibe adzapulumuke kwa Abisalomu.
Tiyeni tichoke msanga, mwina iye adzabwera msanga ndi kutipitirira,
n’kuwononga ife ndi mzinda wathu ndi lupanga.”
15 Akuluakulu a mfumu anamuyankha kuti, “Antchito anu ndi okonzeka
kuchita chilichonse chimene mbuye wathu mfumu mukufuna kuchita.”
16 Mfumu inanyamuka pamodzi ndi banja lake lonse. Koma iye anasiya
azikazi khumi kuti azisamalira nyumba yaufumu. 17 Kotero mfumu
inanyamuka pamodzi ndi anthu onse oyitsatira, ndipo anayima pamalo
pena chapatalipo. 18 Ankhondo ake onse anayamba kuyenda pamaso pa
Davide, ndipo Akereti ndi Apeleti, pamodzinso ndi Agiti okwanira 600
amene anamutsata kuchokera ku Gati, nawonso anayenda pamaso pake.
19 Mfumu inati kwa Itai Mgiti, “N’chifukwa chiyani iwe ukupita ndi
ife? Bwerera ndipo ukakhale ndi mfumu Abisalomu. Iwe ndiwe mlendo
munthu wothawa kwawo. 20 Wangobwera dzulo lomweli, lero ndikutenge
kuti uziyendayenda ndi ife, pamene ine sindikudziwa kumene ndikupita?
Bwerera, ndipo tenga abale ako. Chifundo ndi kukhulupirika zikhale
nawe.”
21 Koma Itai anayankha mfumu kuti, “Pali Yehova wamoyo, kulikonse
kumene mbuye wanga mfumu mudzakhala, kaya ndi moyo kapena imfa,
mtumiki wanu adzakhala komweko.”
22 Davide anati kwa Itai, “Tiye pita nafe” Kotero Itai Mgiti anayenda
pamodzi ndi anthu ake ndi mabanja amene anali naye.
23 Anthu onse a madera ozungulira analira mofuwula pamene anthu
onsewo amadutsa. Mfumunso inawoloka chigwa cha Kidroni, ndipo anthu
onse anayenda kulowera ku chipululu.

24 Zadoki anali nawonso, ndipo Alevi onse amene anali naye ananya-
mula Bokosi la Chipangano la Mulungu. Iwo anayika pansi Bokosi la
Mulungulo ndipo Abiatara ankapereka nsembe mpaka pamene anthu onse
anamaliza kutuluka mu mzinda.
25 Kenaka mfumu inati kwa Zadoki, "Tenga Bokosi la Mulungu ubw-
erere nalo mu mzinda. Ngati ndidzapeza chifundo pamaso pa Yehova,
adzandibweretsa kuti ndilionenso ndi malo ake okhalamo. 26 Koma
iye anati, 'Akapanda kukondwera nane,' chabwino, andichite chimene
chimukomere."
27 Mfumu inatinso kwa wansembe Zadoki, "Kodi siwe mlosi? Bwerera
mu mzinda mwamtendere pamodzi ndi mwana wako Ahimaazi ndi
Yonatani mwana wa Abiatara. Iwe ndi Abiatara tengani ana anu awiri.
28 Ine ndidzadikira powolokera Yorodani ku chipululu mpaka nditalandira
mawu ochokera kwa iwe ondiwuza mmene zilili zinthu." 29 Kotero Zadoki
ndi Abiatara ananyamula Bokosi la Mulungu lija nabwerera nalo ku
Yerusalemu, ndipo anakakhala kumeneko.
30 Koma Davide anapitirira ndi kukakwera phiri la Olivi akupita nalira.
Anafunda kumutu koma sanavale nsapato. Anthu onse amene anali naye
anafundanso kumutu, ndipo nawonso amalira pamene amapita. 31 Tsono
Davide anamva kuti, "Ahitofele ali pakati pa anthu owukira pamodzi ndi
Abisalomu." Choncho Davide anapemphera, "Inu Yehova, musandutse
uphungu wa Ahitofele ukhale uchitsiru."
32 Davide atafika pamwamba pa phiri pomwe anthu ankapembedzerapo
Mulungu, Husai Mwariki anadzakumana naye atang'amba mkanjo wake
ndi kudzithira fumbi kumutu. 33 Davide anati kwa iye, "Ngati iwe upite
ndi ine, udzakhala chondilemetsa. 34 Koma ngati ubwerera ku mzinda ndi
kukanena kwa Abisalomu kuti, 'Inu mfumu ine ndidzakhala wantchito
wanu.' M'mbuyomu ndinali wantchito wa abambo anu koma tsopano
ndidzakhala wantchito wanu. Ukatero udzandithandiza kulepheretsa
malangizo a Ahitofele. 35 Kodi ansembe, Zadoki ndi Abiatara, sakukhala
nawe kumeneko? Ukawawuze zonse zimene umamva m'nyumba yau-
fumu. 36 Ana awo awiri, Ahimaazi wa Zadoki, ndi Yonatani mwana wa
Abiatara ali nawo pamodzi, uzikawatuma kwa ine ndi china chilichonse
chimene ukamve."
37 Ndipo Husai bwenzi la Davide anafika ku Yerusalemu pamene
Abisalomu amalowa mu mzinda.

# 16

*Davide ndi Ziba*

1 Davide atapitirira pang'ono pamwamba pa phiri, anakumana ndi Ziba
mtumiki wa Mefiboseti akudikira kuti akumane naye. Iye anali ndi abulu
a chishalo pa msana ndipo ananyamula malofu a buledi 200, ntchintchi
100 za mphesa zowuma, zipatso za pa nthawi yachilimwe 100 ndi thumba
la vinyo.
2 Mfumu inafunsa Ziba kuti, "N'chifukwa chiyani wabweretsa izi?"
Ziba anayankha kuti, "Abuluwa ndi oti anthu a m'banja mwanu
akwerepo, buledi ndi zipatso ndi za anthu anu kuti adye, ndipo vinyoyo
ndi woti atsitsimutse anthu amene atope m'chipululu."
3 Kenaka mfumu inafunsa kuti, "Kodi chidzukulu cha mbuye wako chili
kuti?"

Ziba anati kwa iye, “Watsalira ku Yerusalemu chifukwa akuganiza kuti,
‘Lero Aisraeli andibwezera ufumu wa agogo anga.’ ”
4 Ndipo mfumu inati kwa Ziba, “Zonse zimene zinali za Mefiboseti ndi
zako tsopano.”
Ziba anati, “Ine modzichepetsa ndikukugwandirani, mbuye wanga
mfumu, kuti ndipeze chisomo pamaso panu.”

### *Simei Atukwana Davide*

5 Mfumu Davide itayandikira Bahurimu, munthu wochokera ku fuko
limodzi ndi banja la Sauli anabwera kuchokera m’menemo. Dzina lake
linali Simei, mwana wa Gera ndipo amatukwana pamene amabwera.
6 Iye amagenda Davide miyala ndi akuluakulu onse a mfumu, ngakhale
kuti ankhondo onse ndi oteteza Davide anali ali kumanzere ndi kumanja
kwake. 7 Potukwana, Simeiyo amati, “Choka iwe, choka iwe, munthu
wopha anthu, munthu wachabechabe iwe! 8 Yehova wakubwezera
chifukwa cha magazi onse amene unakhetsa pa nyumba ya Sauli, yemwe
iwe ukulamulira m’malo mwake. Yehova wapereka ufumu kwa mwana
wako Abisalomu. Ndipo ona mathero ako ndi amenewa chifukwa ndiwe
munthu wopha anthu!”
9 Ndipo Abisai mwana wa Zeruya anati kwa mfumu, “N’chifukwa
chiyani galu wakufa uyu akutukwana mbuye wanga mfumu? Ndiloleni
ndipite kuti ndikadule mutu wake.”
10 Koma mfumu inati, “Inu ana a Zeruya, kodi ndikuchitireni chiyani?
Ngati iye akutukwana chifukwa Yehova wamuwuza kuti, ‘Tukwana
Davide,’ angafunse ndani kuti, ‘N’chifukwa chiyani ukuchita zimenezi?’ ”
11 Tsono Davide anati kwa Abisai ndi akuluakulu ake onse, “Mwana
wanga wobereka ndekha akufuna kundipha. Nanji tsono munthu wa
fuko la Benjamini uyu! Musiyeni; mulekeni atukwane pakuti Yehova
wachita kumuwuza kuti atero. 12 Mwina Yehova adzaona mazunzo anga
ndipo adzandibwezera zabwino chifukwa cha kutukwanidwa kumene
ndikulandira lero.”
13 Kotero Davide ndi anthu ake anapitirira kuyenda mu msewu pamene
Simei amayenda m’mbali mwa phiri moyang’anana naye akutukwana ndi
kuponya miyala pamene amayenda n’kumamutsiranso dothi. 14 Mfumu
ndi anthu ake onse anafika kumene amapita atatopa kwambiri. Ndipo
kumeneko anapumula.

### *Malangizo a Husai ndi Ahitofele*

15 Pa nthawi imeneyi Abisalomu ndi Aisraeli ena onse anabwera ku
Yerusalemu, Ahitofele anali naye. 16 Tsono Husai Mwariki bwenzi la
Davide anapita kwa Abisalomu ndipo anati kwa iye, “Ikhale ndi moyo
wautali mfumu! Ikhale ndi moyo wautali mfumu!”
17 Abisalomu anafunsa Husai, “Kodi ichi ndi chikondi chimene uku-
muonetsa bwenzi lako? N’chifukwa chiyani sunapite ndi bwenzi lako?”
18 Husai anati kwa Abisalomu, “Ayi, ndidzakhala wake wa amene Yehova
wamusankha, wosankhidwa ndi anthu awa ndi anthu onse a Israeli, ndipo
ndidzakhala wake nthawi zonse. 19 Kodi ndidzatumikiranso yani? Kodi
sinditumikira mwana wa mfumu? Monga momwe ndinatumikira abambo
anu, kotero ndidzatumikiranso inu.”
20 Abisalomu anati kwa Ahitofele, “Tiwuze malangizo ako. Kodi tichite
chiyani?”

21 Ahitofele anayankha kuti, “Mugone ndi azikazi a abambo anu amene
awasiya kuti asamalire nyumba yaufumu. Aisraeli onse adzamva kuti
mwachitira abambo anu chinthu chonyansa kotheratu ndipo anthu onse
amene ali ndi iwe adzalimbikitsidwa.” 22 Choncho anamangira tenti
Abisalomu pa denga la nyumba ndipo iye anagona ndi azikazi a abambo
ake Aisraeli onse akuona.

23 Tsono masiku amenewo malangizo amene Ahitofele amapereka anali
ngati mawu ochokera kwa Mulungu. Umu ndi mmene Davide ndi
Abisalomu amalandirira malangizo onse a Ahitofele.

# 17

1 Ahitofele anati kwa Abisalomu, “Mundilole ndisankhe asilikali 12,000,
ndinyamuke usiku womwe uno kuti ndithamangire Davide. 2 Ndipo
ndikamuthira nkhondo atatopa ndiponso atataya mtima. Ndikamuchititsa
mantha ndipo anthu onse amene ali naye akathawa. Ine ndikakantha
mfumu yokhayo, 3 ndipo anthu onse ndidzabwera nawo kwa inu, ngati
mkwati amene akubwerera kwa mwamuna wake. Imfa ya munthu
mmodzi yekha idzakhalitsa anthu onse pa mtendere.” 4 Malangizo awa
anaoneka abwino kwa Abisalomu ndi kwa akuluakulu onse a Israeli.

5 Koma Abisalomu anati, “Muyitanenso Husai Mwariki kuti timve
zimene iye adzanena.” 6 Husai atabwera kwa iye, Abisalomu anati,
“Ahitofele wapereka malangizo ake. Kodi tichite zimene wanena? Ngati
sichoncho, tiwuze maganizo ako.”

7 Husai anayankha Abisalomu kuti, “Malangizo amene Ahitofele
wapereka si abwino pa nthawi ino. 8 Inu mukudziwa bwino abambo anu
ali ndi ankhondo awo. Iwo ndi anthu ankhondo komanso ndi woopsa
ngati chimbalangondo chimene chalandidwa ana ake. Kuwonjezera apa
abambo anu ndi katswiri wa nkhondo. Iwo sanagone pamodzi ndi asilikali
awo. 9 Onani, ngakhale tsopano lino abisala m’phanga lina ku malo ena
ake. Ngati iwo atayamba kuthira nkhondo asilikali anu, aliyense amene
adzamve zimenezi adzati, ‘Gulu lalikulu lankhondo lotsatira Abisalomu
laphedwa.’ 10 Tsono ngakhale msilikali wolimba mtima kwambiri, amene
mtima wake uli ngati wa mkango, adzagwidwa ndi mantha aakulu pakuti
Aisraeli akudziwa kuti abambo anu ndi ankhondo ndipo kuti iwo amene
ali nawo ndi anthu olimba mtima.

11 “Kotero ine ndikukulangizani kuti: Aisraeli onse, kuchokera ku Dani
mpaka ku Beeriseba; ochuluka ngati mchenga wa m’mbali mwa nyanja,
asonkhane kwa inu ndipo muwatsogolera kupita ku nkhondo. 12 Ndipo
ife tidzapita kukamuthira nkhondo kulikonse kumene tikamupeze, ndipo
ife tikamuthira nkhondo ngati mame pa nthaka. Palibe amene adzakhale
wamoyo kaya iye kapena ankhondo ake. 13 Iye akakathawira mu mzinda,
Aisraeli onse adzabweretsa zingwe ku mzindawo, ndipo ife tidzawugwet-
sera ku chigwa mpaka sipadzapezeka ngakhale kachidutswa.”

14 Abisalomu ndi ankhondo ena onse a Israeli anati, “Malangizo a Husai
Mwariki ndi abwino kuposa a Ahitofele.” Pakuti Yehova anatsimikiza
kutsutsa malangizo onse abwino a Ahitofele ndi cholinga choti zimuvute
Abisalomu.

15 Husai anawuza ansembe Zadoki ndi Abiatara kuti, “Ahitofele analan-
giza Abisalomu ndi akuluakulu a Israeli zakuti, koma ine ndawalangiza
kuchita zakutizakuti. 16 Tsopano tumizani wamthenga msangamsanga
kuti akamuwuze Davide kuti, ‘Musakagone powolokera Yorodani ku

chipululu koma mukawoloke. Mukapanda kutero, mfumu ndi anthu onse
amene ali naye adzaphedwa.' "

17 Yonatani ndi Ahimaazi amakhala ku Eni Rogeli. Tsono wantchito
wamkazi ndiye amapita kukawawuza ndipo iwo amayenera kupita kuka-
muwuza mfumu Davide, pakuti iwowo sankayenera kuonekera polowa
mu mzinda. 18 Koma mnyamata wina anawaona ndipo anakawuza
Abisalomu. Kotero anthu awiriwo anachoka mofulumira ndipo anapita ku
nyumba ya munthu wina ku Bahurimu. Iye anali ndi chitsime ku mpanda
kwake ndipo iwo analowamo. 19 Mkazi wake anatenga chophimba ndipo
anachiyika pamwamba pa chitsimecho nawazapo tirigu. Palibe amene
anadziwa chilichonse za izi.
20 Anthu a Abisalomu atafika kwa mkaziyo pa nyumbapo anafunsa kuti,
"Kodi Ahimaazi ndi Yonatani ali kuti?"

Mkaziyo anawayankha kuti, "Awoloka mtsinje." Anthuwo anafunafuna
koma sanapeze munthu, kotero anabwerera ku Yerusalemu.

21 Anthu aja atapita, awiriwo anatuluka m'chitsimemo ndipo anapita
kukawuza mfumu Davide nati kwa iye, "Nyamukani, muwoloke mtsinje
msangamsanga. Ahitofele wapereka malangizo akutiakuti kutsutsana
nanu." 22 Kotero Davide ndi anthu onse amene anali nawo ananyamuka
ndi kuwoloka Yorodani. Pofika mmamawa, panalibe munthu amene
anatsala asanawoloke Yorodani!
23 Ahitofele ataona kuti malangizo ake sanatsatidwe, iye anakwera bulu
wake napita ku mzinda wa kwawo ku nyumba yake. Iye anakonza
m'nyumba mwakemo ndi kudzimangirira. Kotero anafa nayikidwa
m'manda a abambo ake.
24 Davide anapita ku Mahanaimu, ndipo Abisalomu anawoloka Yorodani
pamodzi ndi ankhondo ena onse a Israeli. 25 Abisalomu anasankha
Amasa kukhala mkulu wa ankhondo m'malo mwa Yowabu. Amasa
anali mwana wa munthu wotchedwa Itira Mwisraeli amene anakwatira
Abigayeli mwana wa Nahasi mlongo wake wa Zeruya, amayi ake a
Yowabu. 26 Aisraeli ndi Abisalomu anamanga zithando m'dziko la Giliyadi.

27 Davide atafika ku Mahanaimu, Sobi mwana wa Nahasi wochokera
ku Raba ku dziko la Amoni ndi Makiri mwana wa Amieli wochokera ku
Lodebara, ndi Barizilai Mgiliyadi wochokera ku Rogelimu 28 anabweretsa
zofunda, mabeseni ndi miphika. Iwo anabweretsanso kwa Davide ndi
anthu ake zakudya izi: tirigu ndi barele, ufa ndi tirigu wokazinga, nyemba
ndi mphodza, 29 uchi ndi chambiko, nkhosa ndi mafuta olimba a mkaka
wang'ombe. Pakuti anati, "Anthuwa ali ndi njala ndipo atopa, alinso ndi
ludzu muno m'chipululu."

# 18

*Imfa ya Abisalomu*

1 Davide anasonkhanitsa anthu amene anali naye ndipo anasankha
atsogoleri ena olamulira ankhondo 1,000 ndi ena olamulira ankhondo
100. 2 Davide anatumiza asilikaliwo atawagawa patatu: gulu loyamba
limalamulidwa ndi Yowabu, gulu lachiwiri limalamulidwa ndi Abisai
ndipo gulu lachitatu limalamulidwa ndi Itai Mgiti. Mfumu inawuza
asilikaliwo kuti, "Inenso ndipita nanu ndithu."

3 Koma anthuwo anati, "Inu musapite nafe. Ngati tidzathamangitsidwa,
iwowo sadzasamala za ife. Ngakhale theka la ife litafa, iwo sadzasamalako.

Koma inuyo ndinu ofunika kuposa asilikali 10,000. N'kwabwino kwambiri kuti inu muzititumizira chithandizo kuchokera ku mzindako."

4 Mfumu inayankha kuti, "Ine ndichita chimene chili chokukomerani."

Kotero mfumu inayima pambali pa chipata pamene ankhondo onse
amayenda m'magulu a anthu 100 ndi a 1,000. 5 Mfumu inalamulira
Yowabu, Abisai ndi Itai kuti, "Mumukomere mtima Abisalomu chifukwa cha ine." Ndipo asilikali onse anamva pamene mfumu imalamula izi za Abisalomu kwa wolamulira aliyense.

6 Ankhondo anayenda kupita kukachita nkhondo ndi Israeli, ndipo
nkhondo inachitika m'nkhalango ya Efereimu. 7 Aisraeli anagonjetsedwa
kumeneko ndi ankhondo a Davide. Tsiku limenelo anaphedwa anthu
okwanira 20,000. 8 Nkhondo inafalikira ku madera onse akumidzi ndipo anthu akufa chifukwa cha zoopsa za m'nkhalango anali ambiri tsiku limenelo kuposa akufa ndi lupanga.

9 Tsono zinachitika kuti Abisalomu anakumana ndi asilikali a Davide. Iye anali atakwera bulu ndipo pamene buluyo amadutsa pansi pa nthambi zambiri za mtengo wa thundu, mutu wa Abisalomu unakodwa mu mtengomo. Iye anasiyidwa atatsakamira m'malele, pamene bulu amene anakwerapoyo amapitirira.

10 Mmodzi mwa asilikali ataona zimenezi, anamuwuza Yowabu kuti, "Ine ndamuona Abisalomu ali lende mu mtengo wa thundu."

11 Yowabu anati kwa munthu amene anamuwuza zimenezi, "Ukuti chiyani! Unamuona? N'chifukwa chiyani sunamukanthire pansi pomwepo? Ndipo ine ndikanakupatsa ndalama za siliva khumi ndi lamba wausilikali."

12 Koma munthuyo anayankha kuti, "Ngakhale atandipatsa m'manja mwanga ndalama zasiliva 1,000, sindingatambasule dzanja langa kupha mwana wa mfumu. Ife tikumva, mfumu inalamula inu Abisai ndiponso
Itai kuti, 'Mutetezeni mnyamatayo Abisalomu chifukwa cha ine!' 13 Ndipo
sindikanayika moyo wanga pa chiswe pakuti palibe chimene chimabisika pamaso pa mfumu komanso inu simukanditeteza."

14 Yowabu anati, "Ine sinditayanso nthawi ndi iwe." Ndipo anatenga mikondo itatu m'manja mwake ndipo anabaya pamtima pa Abisalomu,
Abisalomuyo akanali ndi moyo pa mtengo wa thundu. 15 Ndipo anthu
khumi onyamula zida za Yowabu anazungulira Abisalomu, kumubaya ndi kumupha.

16 Kenaka Yowabu analiza lipenga ndipo asilikali analeka kuthamangitsa
Israeli pakuti Yowabu anawaletsa. 17 Iwo anatenga Abisalomu ndi
kumuponya m'dzenje lalikulu m'chipululumo ndipo anawunjikapo miyala ikuluikulu. Nthawiyi Aisraeli onse anathawa kupita ku nyumba zawo.

18 Abisalomu ali ndi moyo anadzimangira chipilala m'chigwa cha mfumu, pakuti ankaganiza kuti, "Ine ndilibe mwana wamwamuna amene adzakhale chikumbutso changa." Chipilalacho anachitchula dzina lake lomwe ndipo mpaka lero chimatchedwa chipilala cha Abisalomu.

### *Davide Alira Abisalomu*

19 Tsono Ahimaazi mwana wa Zadoki anati, "Ndiloleni ndithamange ndi kukapereka uthenga kwa mfumu kuti Yehova wayipulumutsa m'dzanja la adani ake."

20 Yowabu anamuwuza iye kuti, "Iwe si amene uti ukanene zimenezi lero. Ukapereka uthenga nthawi ina, koma usatero lero, chifukwa mwana wa mfumu wafa."

21 Kenaka Yowabu anawuza Mkusi kuti, “Pita ukawuze mfumu zimene
waona.” Mkusiyo anawerama pamaso pa Yowabu ndipo anathamanga
kupita.
22 Ahimaazi mwana wa Zadoki ananenanso kwa Yowabu kuti, “Zivute
zitani, chonde mundilole kuti ndipite pambuyo pa Mkusiyo.”
Koma Yowabu anayankha kuti, “Mwana wanga, n’chifukwa chiyani
ukufuna kupita? Ulibe nkhani yoti ukalandire nayo mphotho.”
23 Iye anati, “Zivute zitani ine ndikufuna kuti ndipite.”
Choncho Yowabu anati “Pita!” Ndipo Ahimaazi anathamanga kudzera
njira ya ku chigwa ndipo anamupitirira Mkusi uja.
24 Nthawi imeneyo n’kuti Davide atakhala pakati pa zipata ziwiri,
chakubwalo ndi cham’kati. Mlonda anakwera pa khoma nakayimirira
pa denga la chipata. Anati atayang’ana, anaona munthu akuthamanga
yekhayekha. 25 Mlonda uja anapita kwa mfumu ndipo anafotokoza.
Mfumu inati, “Ngati ali yekha ali ndi nkhani yabwino” Ndipo munthuyo
anayandikira.
26 Mlonda uja anaonanso munthu wina akuthamanga, ndipo anayitana
woyang’anira pa chipata, “Taona, munthu winanso akuthamanga ali
yekha!”
Mfumu inati, “Iye akubweretsanso nkhani yabwino.”
27 Mlonda uja anati, “Munthu akuthamanga patsogoloyo,
kathamangidwe kake kakufanafana ndi mmene amathamangira
Ahimaazi, mwana wa Zadoki.”
Mfumu inati, “Ameneyo ndi munthu wabwino, ndipo akubwera ndi
nkhani yabwino.”
28 Ndipo Ahimaazi anafuwula kwa mfumu, “Zonse zili bwino!” Iye
anagwada pamaso pa mfumu nkhope yake atagunditsa pansi ndipo anati,
“Yehova Mulungu wathu alemekezedwe! Iye wapereka m’dzanja lathu
anthu amene anawukira inu mbuye wanga mfumu.”
29 Mfumu inafunsa, “Kodi mnyamata uja Abisalomu watetezedwa?”
Ahimaazi anayankha, “Pamene Yowabu amati azindituma ine mtu-
miki wanu ndinaona chipiringu cha anthu, koma sindikudziwa chinali
chiyani.”
30 Mfumu inati, “Ima apo ndipo udikire.” Kotero iye anapita pa mbali
nayima pamenepo.
31 Kenaka Mkusi uja anafika ndipo anati, “Mbuye wanga mfumu imvani
nkhani yabwino! Yehova wakupulumutsani inu lero kwa onse amene
anakuwukirani.”
32 Mfumu inafunsa Mkusiyo kuti, “Kodi mnyamata uja Abisalomu
watetezedwa?”
Mkusiyo anayankha kuti, “Adani anu mbuye wanga mfumu, pamodzi
ndi anthu onse amene amakuwukirani, ziwaonekere zomwe zamuonekera
mnyamatayo.”
33 Mfumu inanthunthumira. Inapita ku chipinda cha mmwamba cha pa
chipata kukalira. Pamene imapita, inkati: “Iwe mwana wanga Abisalomu!
Mwana wanga! Mwana wanga Abisalomu! Zikanakhala bwino ndikanafa
ndine m’malo mwako! Iwe Abisalomu, mwana wanga, mwana wanga!”

# 19

1 Yowabu anawuzidwa kuti, “Mfumu ikulira maliro a Abisalomu.”
2 Ndipo kwa asilikali onse chipambano cha tsiku limenelo chinasandulika
maliro, chifukwa tsiku limenelo anthu anamva kuti mfumu ili pa chisoni

chachikulu chifukwa cha mwana wake. 3 Ankhondo analowa mu
mzinda mwakachetechete tsiku limenelo ngati momwe amalowera anthu
mwamanyazi chifukwa athawa ku nkhondo. 4 Mfumu inaphimba nkhope
yake ndipo inalira mofuwula, “Iwe mwana wanga Abisalomu! Iwe
Abisalomu, mwana wanga, mwana wanga!”

5 Kenaka Yowabu analowa m’nyumba ya mfumu nafika kwa mfumuyo
ndipo anati, “Lero mwachititsa manyazi asilikali anu onse, amene
apulumutsa moyo wanu ndiponso moyo wa ana anu aamuna ndi aakazi,
kudzanso moyo wa akazi anu ndi wa azikazi anu. 6 Inu mumakonda
amene amadana nanu ndipo mumadana ndi amene amakukondani.
Inuyo mwaonetsa lero poyera kuti simusamala za atsogoleri anu a
nkhondo ndi asilikali awo. Ine ndikuona kuti inu mukanakondwera
ngati Abisalomu akanakhala ndi moyo lero, tonsefe titafa. 7 Tsopano
pitani mukawalimbikitse asilikali anu. Ine ndikulumbira mwa Yehova
kuti ngati inu simupita palibe munthu amene adzatsale ali ndi inu polowa
dzuwa. Ichi chidzakhala choyipa kwambiri kuposa zovuta zonse zimene
zinakugwerani kuyambira muli mnyamata mpaka lero.”

8 Kotero mfumu inanyamuka ndipo inakhala pa mpando wake pa
chipata. Pamene asilikali anawuzidwa kuti, “Mfumu yakhala pa chipata,”
onse anabwera kwa iye.

### *Davide Abwerera ku Yerusalemu*

Nthawi imeneyi n’kuti Aisraeli atathawira ku nyumba zawo. 9 Pakati
pa mafuko onse a Israeli, anthu amakangana ndipo amati, “Mfumu
inatipulumutsa m’manja mwa adani anthu. Iye ndi amene anatilanditsa
m’dzanja la Afilisti. Koma tsopano wathawa m’dziko muno chifukwa cha
Abisalomu. 10 Ndipo Abisalomu amene ife tinamudzoza kuti atilamulire
wafa pa nkhondo. Tsono n’chifukwa chiyani simukunena kanthu za
kubweretsanso mfumu?”

11 Mfumu Davide inatumiza uthenga uwu kwa ansembe Zadoki ndi Abi-
atara, “Funsani akuluakulu a Yuda, ‘N’chifukwa chiyani inu mukukhala
otsiriza kuyitana mfumu ku nyumba yake yaufumu, pakuti zimene
zikunenedwa mu Israeli yense zamveka kwa mfumu ndi onse amene
akukhala nayo. 12 Inu ndinu abale anga enieni, mafupa anga ndi
mnofu wanga. N’chifukwa chiyani inuyo mukukhala otsiriza kubweretsa
mfumu?’ 13 Ndipo munene kwa Amasa, ‘Kodi iwe si m’bale wanga
weniweni? Mulungu andilange, andilange kwambiri ngati kuyambira
tsopano sukhala mtsogoleri wa ankhondo anga kulowa m’malo mwa
Yowabu.’ ”

14 Davide anakopa mitima ya anthu onse a Yuda ndipo anthuwo
anakhala ngati munthu mmodzi. Iwo anatumiza mawu kwa mfumu,
“Bwererani inu ndi anthu anu onse.” 15 Kotero mfumu inabwerera ndipo
inakafika mpaka ku Yorodani.

Tsono anthu a ku Yuda anabwera ku Giligala kuti akakumane ndi
mfumu ndi kumuwolotsa Yorodani. 16 Simei mwana wa Gera, wa fuko
la Benjamini wa ku Bahurimu, anabwera mofulumira pamodzi ndi Ayuda
kudzakumana ndi mfumu Davide. 17 Iyeyo anali ndi anthu 1,000 a fuko
la Benjamini pamodzi ndi Ziba, wantchito wa banja la Sauli ndi ana
ake aamuna khumi ndi asanu ndi antchito ake makumi awiri. Iwo
anathamangira ku Yorodani kumene kunali mfumu. 18 Iwo anawoloka
mtsinje kukatenga banja lonse la mfumu ndi kuchita zonse zimene
mfumuyo imafuna.

Pamene Simei mwana wa Gera anawoloka Yorodani, anagwa pansi
chafufumimba pamaso pa mfumu, 19 ndipo anati, “Mbuye wanga
musaganizire za kulakwa kwanga. Musakumbukire zolakwa zimene mtu-
miki wanu anakuchitirani tsiku limene mbuye wanga mfumu mumachoka
mu Yerusalemu. Mfumu musazikumbukirenso zimenezi. 20 Pakuti ine
mtumiki wanu ndazindikira kuti ndachimwa. Koma lero ndabwera ngati
woyamba wa nyumba ya Yosefe yonse kudzakumana nanu mbuye wanga
mfumu.”

21 Ndipo Abisai mwana wa Zeruya anati, “Kodi Simei saphedwa
chifukwa cha ichi? Iye anatukwana wodzozedwa wa Yehova.”

22 Davide anayankha kuti, “Kodi inu ana a Zeruya, ndikuchitireni
chiyani? Lero lino iwe wakhala mdani wanga! Kodi wina aphedwe lero
mu Israeli? Kodi ine sindikudziwa kuti lero ndine mfumu mu Israeli?”
23 Ndipo mfumu inati kwa Simei, “Iwe Simei suphedwa.” Ndipo mfumuyo
inalonjeza ndi lumbiro.

24 Mefiboseti, mdzukulu wa Sauli, nayenso anabwera kudzakumana ndi
mfumu. Kuyambira tsiku limene mfumu inachoka mpaka tsiku limene
inabwerera mu mtendere, iye sanasambe mapazi kaya kumeta ndevu
kapena kuchapa zovala zake. 25 Pamene anafika kuchokera ku Yerusalemu
kudzakumana ndi mfumu, mfumu inamufunsa kuti, “N’chifukwa chiyani
sunapite nane Mefiboseti?”

26 Iye anayankha kuti, “Mbuye wanga mfumu, pakuti ine wantchito
wanu ndine wolumala. Ndinati, ‘Andikonzere chishalo cha bulu wanga
ndipo ndidzakwera kuti ndipite ndi mfumu.’ Koma Ziba wantchito wanga
anandilakwitsa. 27 Ndipo wayankhula zosinjirira za ine mtumiki wanu
kwa inu mbuye wanga mfumu. Mbuye wanga mfumu ali ngati mngelo
wa Mulungu ndipo chitani chimene chikukomerani. 28 Zidzukulu zonse
za agogo anga sizinayenera chilichonse koma imfa kuchokera kwa inu
mbuye wanga mfumu, koma inu munapereka malo kwa mtumiki wanu
pakati pa amene amadya pa tebulo lanu. Tsono ine ndili ndi chiyaninso
kuti ndipitirize kudandaula kwa mfumu?”

29 Mfumu inayankha kuti, “Uneneranji zambiri? Ine ndikulamula kuti
iwe ndi Ziba mugawane minda.”

30 Mefiboseti anati kwa mfumu, “Mululeni atenge zonse, pakuti tsopano
mbuye wanga mwafika kwanu mu mtendere.”

31 Barizilai Mgiliyadi anabweranso kuchokera ku Rogelimu kudza-
woloka Yorodani ndi mfumu ndi kumuperekeza kuchokera kumeneko.
32 Tsono Barizilai anali wokalamba kwambiri, wa zaka makumi asanu
ndi atatu. Iye ndi amene anapereka zinthu kwa mfumu pamene anali
ku Mahanaimu pakuti anali wolemera kwambiri. 33 Mfumu inati kwa
Barizilai, “Woloka nane ndipo ukakhale ndi ine mu Yerusalemu ndipo
ineyo ndidzakusamalira.”

34 Barizilai anayankha mfumu kuti, “Kodi zakhala zaka zingati zoti
ndikhale ndi moyo, kuti ndipite ku Yerusalemu ndi mfumu? 35 Ine
tsopano ndili ndi zaka 80. Kodi ndingathe kusiyanitsa pakati pa chabwino
ndi choyipa? Kodi mtumiki wanu angathe kuzindikira kukoma kwa
zimene akudya ndi kumwa? Kodi ndingathe kumva kuyimba kwa
amuna ndi akazi? N’chifukwa chiyani wantchito wanu akakhale ngati
katundu kwa mbuye wanga mfumu? 36 Koma ine mtumiki wanu
ndingoyenda pang’ono kuti ndiwoloke Yorodani pamodzi ndi mfumu.

Amfumu mungandipatsirenji mphotho yotere? 37 Muloleni, mtumiki
wanu abwerere, kuti ndikafere kwathu pafupi ndi manda a abambo
ndi amayi anga. Koma nayu mtumiki wanu Kimuhamu. Muloleni iye
awoloke nanu mbuye wanga mfumu. Mumuchitire chilichonse chimene
chikukomereni!”

38 Mfumu inati, “Kimuhamu adzawoloka ndi ine, ndipo ndidzamuchitira
iye chilichonse chimene chidzakondweretsa iwe. Ndipo chilichonse
chimene udzandipempha ine ndidzakuchitira.”

39 Kotero anthu onse anawoloka Yorodani ndipo kenaka mfumu ina-
woloka. Mfumu inapsompsona Barizilai ndi kumupatsa madalitso ndipo
Barizilaiyo anabwerera kwawo.

40 Pamene mfumu inawolokera ku Giligala, Kimuhamu anawoloka naye.
Ankhondo onse a Yuda ndi theka la ankhondo a Israeli onse anaperekeza
mfumu.

41 Kenaka Aisraeli onse amabwera kwa mfumu n’kumati kwa iye,
“N’chifukwa chiyani abale athu, anthu a ku Ayuda, anakubani mfumu,
nawoloka nanu Yorodani inu ndi banja lanu, pamodzi ndi anthu ake
onse?”

42 Ayuda onse anayankha Aisraeli kuti, “Ife timachita zimenezi chifukwa
mfumu ndi m’bale wathu. N’chifukwa chiyani inu mwapsa mtima ndi
zimenezi? Kodi ife tinadya chakudya chilichonse cha mfumu? Kodi chilipo
chimene ife tatenga kukhala chathu?”

43 Aisraeli anayankha Ayuda kuti, “Ife ndi magawo khumi mwa mfumu
imeneyi, ndipo kuwonjezera apo, ife tili ndi zinthu zambiri mwa Davide
kuposa inu. Tsono n’chifukwa chiyani mukutichita chipongwe? Kodi ife
si amene tinayamba kunena za kubweretsa mfumu yathu?”

Koma anthu a Yuda anayankha mwaukali kwambiri kupambana anthu
a ku Israeli.

# 20

*Seba Awukira Davide*

1 Ndipo munthu wina wokonda kuyambitsa chisokonezo, dzina lake
Seba, mwana wa Bikiri wa fuko la Benjamini, anali komweko. Iye analiza
lipenga ndipo anafuwula kuti,

“Ife tilibe chathu mu mfumu wa Davide,
tilibe gawo mwa mwana wa Yese!
Inu Aisraeli aliyense apite ku nyumba kwake!”

2 Kotero Aisraeli onse anamuthawa Davide ndipo anatsatira Seba
mwana wa Bikiri. Koma anthu a ku Yuda anakhala ndi mfumu yawo
njira yonse kuchokera ku Yorodani mpaka ku Yerusalemu.

3 Davide atabwerera ku nyumba yake yaufumu ku Yerusalemu, iye
anatenga azikazi khumi aja amene anawasiya kuti aziyang’anira nyumba
yaufumu, ndipo anawayika m’nyumba imene anayikapo mlonda. Iye
ankawadyetsa koma sanagone nawonso. Anasungidwa kwa okha mpaka
tsiku la kufa kwawo ndipo anakhala ngati akazi amasiye.

4 Kenaka mfumu inati kwa Amasa, “Itanitsa ankhondo a Yuda kuti
abwere kwa ine pasanathe masiku atatu, ndipo iwe udzakhale nawo.”
5 Motero Amasa anakayitana Ayuda, koma anachedwa, napitirira pa
nthawi imene mfumu inamuyikira.

6 Davide anati kwa Abisai, “Tsono Seba mwana wa Bikiri adzatipweteka
kuposa momwe Abisalomu anatichitira. Tenga asilikali a mbuye wako

ndipo umuthamangitse, mwina adzapeza mizinda yotetezedwa ndi ku-
tithawa ife." 7 Kotero anthu a Yowabu, Akereti ndi Apeleti ndiponso
asilikali onse amphamvu anapita motsogozedwa ndi Abisai. Iwo anayenda
kuchokera ku Yerusalemu kuthamangitsa Seba mwana wa Bikiri.

8 Ali pa mwala waukulu wa ku Gibiyoni, Amasa anabwera kudzakumana
nawo. Yowabu anali atavala chovala chausilikali ndipo pamwamba pa
malayawo, m'chiwuno mwake anavala lamba womangirirapo lupanga lili
moyikamo mwakemo. Akuyenda linasololoka kuchoka moyikamo mwake.

9 Yowabu anati kwa Amasa, "Kodi uli bwanji m'bale wanga?" Kenaka
Yowabu anamugwira ndevu Amasa uja ndi dzanja lake lamanja ndi kup-
sompsona. 10 Amasa sanayang'anitsitse lupanga limene linali m'dzanja
la Yowabu, ndipo Yowabu anamubaya nalo m'mimba ndipo matumbo
ake anatuluka ndi kugwera pansi. Popanda kubayanso kachiwiri, Amasa
anafa. Ndipo Yowabu ndi m'bale wake Abisai anathamangitsa Seba
mwana wa Bikiri.

11 Mmodzi mwa ankhondo a Yowabu anakayimirira pafupi ndi mtembo
wa Amasa ndipo anati, "Aliyense amene amakonda Yowabu ndi aliyense
amene ali wa Davide, atsatire Yowabu!" 12 Amasa anagona pakati pa
msewu atasamba magazi ake, ndipo munthuyo anaona kuti asilikali onse
amayima pamenepo. Atazindikira kuti aliyense amene ankafika pamene
panali Amasa amayima, iye anamuchotsa mu msewu ndi kumukokera
m'munda ndipo anamuphimba ndi nsalu. 13 Amasa atachotsedwa pa
msewu anthu onse anapita ndi Yowabu kuthamangitsa Seba mwana wa
Bikiri.

14 Seba anadutsa mafuko onse a Israeli mpaka ku Abeli ndi Beti-Maaka
ndiponso chigawo chonse cha Abeli, amene anasonkhana pamodzi ndi
kumutsata iye. 15 Ankhondo onse pamodzi ndi Yowabu anafika ndi
kumuzungulira Seba mu Abeli-Beti-Maaka. Iwo anapanga mzere wa
nkhondo mpaka ku mzinda, ndipo unayang'anana ndi malo otetezera
a kunja. Pamene amalimbana ndi khoma kuti aligwetse, 16 mayi wina
wanzeru anafuwula kuchokera mu mzindawo, "Tamverani! Tamverani!
Muwuzeni Yowabu abwere pano kuti ndiyankhule naye." 17 Yowabu
anayandikira kumene kunali mayiyo, ndipo iye anafunsa kuti, "Kodi ndinu
Yowabu?"

Iye anayankha kuti, "Ndine."

Mayiyo anati, "Tamverani zimene mtumiki wanu akuti anene."

Yowabu anayankha kuti, "Ndikumvetsera."

18 Iye anapitiriza kunena kuti, "Kalekale ankanena kuti, 'Kapeze yankho
lako ku Abeli,' ndipo nkhani imathera pamenepo. 19 Ife ndife anthu a
mtendere ndi okhulupirika mu Israeli. Inu mukufuna kuwononga mzinda
umene ndi mayi mu Israeli. N'chifukwa chiyani mukufuna kufafaniza
cholowa cha Yehova?"

20 Yowabu anayankha kuti, "Ayi ndisatero. Ine sindikufuna kuwu-
fafaniza kapena kuwuwononga. 21 Nkhani simeneyo ayi. Koma munthu
wina wa ku dziko lamapiri la Efereimu, dzina lake Seba mwana wa Bikiri,
wawukira mfumu Davide. Muperekeni munthuyo ndipo ine ndidzachoka
pa mzinda uno."

Mayiyo anati kwa Yowabu, "Mutu wake tikuponyerani pa khoma pano."

22 Ndipo mayiyo anapita kwa anthu onse ndi malangizo ake anzeru,
ndipo anadula mutu wa Seba mwana wa Bikiri ndipo anawuponya
kwa Yowabu. Kotero iye analiza lipenga ndipo anthu ake anachoka pa

mzindawo, aliyense n'kubwerera kwawo. Ndipo Yowabu anabwerera kwa
mfumu ku Yerusalemu.
23 Yowabu ndiye amalamulira gulu lonse la ankhondo. Benaya mwana
wa Yehoyada amalamulira Akereti ndi Apeleti. 24 Adoramu amayang'anira
anthu ogwira ntchito ya thangata, Yehosafati mwana wa Ahiludi anali
mlembi wa zochitika, 25 Seva anali mlembi wa mfumu. Zadoki ndi
Abiatara anali ansembe 26 ndipo Ira wa ku Yairi anali wansembe wa
Davide.

# 21

*Agibiyoni Abwezera*

1 Pa nthawi ya ulamuliro wa Davide kunali njala kwa zaka zitatu
zotsatana. Kotero Davide anapemphera kwa Yehova. Yehova anati,
"Izi zachitika chifukwa chakuti Sauli ndi banja lake akanali ndi mlandu
wakupha Agibiyoni."
2 Mfumu inayitanitsa Agibiyoni ndipo inayankhula nawo. (Tsono
Agibiyoni sanali Aisraeli, koma otsala mwa Aamori. Aisraeli analumbira
kuwasiya ndi moyo, koma Sauli chifukwa cha chikondi cha pa Israeli
ndi Yuda, anafuna kuwawonongeratu). 3 Davide anafunsa Agibiyoni kuti,
"Kodi ine ndikuchitireni chiyani? Ndipepese bwanji kuti inu mudalitse
cholowa cha Yehova?"
4 Agibiyoni anamuyankha kuti, "Ife tilibe ufulu woti n'kulamula Sauli
ndi banja lake kuti atipatse siliva kapena golide, tilibenso ufulu woti
n'kupha wina aliyense mu Israeli."
Davide anafunsa, "Mukufuna ine ndikuchitireni chiyani?"
5 Iwo anayankha mfumu kuti, "Tsono za munthu amene anatiwononga
ndi kukonza chiwembu choti titheretu ndi kukhala wopanda malo mu
Israeli, 6 mutipatse adzukulu ake aamuna asanu ndi awiri kuti tiwaphe
ndi kuwapereka pamaso pa Yehova ku Gibeya wa Sauli, wosankhidwa wa
Yehova."
Choncho mfumu inati, "Ine ndidzakupatsani."
7 Koma mfumu inasunga Mefiboseti mwana wa Yonatani, mwana wa
Sauli, chifukwa cha kulumbira kumene mfumu Davide ndi Yonatani
mwana wa Sauli anachita pamaso pa Yehova. 8 Ndipo mfumu inatenga
Arimoni ndi Mefiboseti, ana aamuna awiri a Rizipa, mwana wamkazi
wa Ayiwa, amene anaberekera Sauli pamodzi ndi ana asanu a Merabi
mwana wamkazi wa Sauli, amene anabereka Adirieli mwana wa Barizilai
Mmeholati. 9 Iye anawapereka kwa anthu a ku Gibiyoni, amene anawapha
nawayika pa phiri la Yehova. Onse asanu ndi awiri anafera limodzi. Iwo
anaphedwa masiku oyamba kukolola barele.
10 Rizipa mwana wamkazi wa Ayiwa anatenga chiguduli ndi kudziyalira
pa mwala (pamene panali mitemboyo). Kuyambira nthawi yoyamba
kukolola mpaka pamene mvula inayambanso kugwa, iye sanalole kuti
mbalame zikhudze mitemboyo masana kapena nyama zakuthengo usiku.
11 Davide atawuzidwa zimene Rizipa mwana wamkazi wa Ayiwa, mzikazi
wa Sauli anachita, 12 anapita kukatenga mafupa a Sauli ndi mwana wake
Yonatani kwa anthu a ku Yabesi Giliyadi (iwo anawatenga mwamseri
kuchoka pabwalo la ku Beti-Sani, kumene Afilisti anawapachika atapha
Sauli ku Gilibowa). 13 Davide anakatenga mafupa a Sauli ndi mwana
wake Yonatani kumeneko ndiponso mafupa otayidwa a amene anaphedwa
nawasonkhanitsa pamodzi.

14 Iwo anayika mafupa a Sauli ndi mwana wake Yonatani m'manda a
Kisi abambo ake a Sauli ku Zera m'dziko la Benjamini, ndipo anachita
zonse zimene mfumu inalamula. Atachita zimenezi, Mulungu anayankha
pemphero lopempherera dzikolo.

### *Nkhondo ndi Afilisti*

15 Nthawi inanso panali nkhondo pakati pa Afilisti ndi Aisraeli, Davide
anapita ndi ankhondo ake kukamenyana ndi Afilisti ndipo iye anatopa
kwambiri. 16 Ndipo Isibi-Benobi, mmodzi mwa zidzukulu za Rafa, amene
mkondo wake unkalemera makilogalamu atatu ndi theka ndipo analinso
ndi lupanga latsopano, anati adzapha Davide. 17 Koma Abisai mwana wa
Zeruya anabwera kudzapulumutsa Davide. Iye anamukantha Mfilisitiyo
ndi kumupha. Pamenepo asilikali a Davide analumbira kwa iye kuti, "Inu
simudzapita nafenso ku nkhondo, kuti nyale ya Israeli isadzazimitsidwe."
18 Patapita nthawi, panali nkhondo ina ndi Afilisti ku Gobu. Pa nthawi
imeneyo Sibekai Mhusati anapha Safu, mmodzi mwa zidzukulu za Arefai.
19 Pa nkhondo inanso ndi Afilisti ku Gobu, Elihanani mwana wa Yaare-
Oregimu wa ku Betelehemu anapha Goliati Mgiti, amene anali ndi mkondo
ngati ndodo yowombera nsalu.
20 Pa nkhondo inanso imene inachitika ku Gati panali munthu wina
wamtali kwambiri wa zala zisanu ndi chimodzi m'manja ndi m'mapazi
ndipo zonse pamodzi zinalipo 24. Iyenso anali chidzukulu cha Rafa.
21 Pamene iye ankanyoza Aisraeli, Yonatani mwana wa Simea, m'bale
wake wa Davide anamupha.
22 Anthu anayi amenewa anali zidzukulu za Rafa ku Gati, ndipo onse
anaphedwa ndi Davide ndi ankhondo ake.

# 22

### *Nyimbo ya Mayamiko ya Davide*

1 Davide anayimbira Yehova nyimbo iyi pamene Yehovayo anamupulu-
mutsa m'dzanja la adani ake onse ndiponso m'dzanja la Sauli. 2 Iye anati,
"Yehova ndiye thanthwe langa, chitetezo changa ndi mpulumutsi wanga.
3 Mulungu wanga ndiye thanthwe langa, m'mene ndimathawiramo,
chishango changa ndi ndodo yachipulumutso changa.
Iye ndi linga langa, pothawirapo panga ndi mpulumutsi wanga.
Munandipulumutsa m'manja mwa anthu ankhanza.

4 "Ndimayitana Yehova amene ndi woyenera matamando,
ndipo ndapulumutsidwa kwa adani anga.

5 "Mafunde a imfa anandizinga;
mitsinje yothamanga yachiwonongeko inandiopsa kwambiri.
6 Anandimanga ndi zingwe za ku manda;
misampha ya imfa inalimbana nane.

7 "M'masautso anga ndinapemphera kwa Yehova;
ndinapemphera kwa Mulungu wanga.
Iye ali m'nyumba yake, anamva mawu anga;
kulira kwanga kunafika m'makutu ake.

8 "Dziko lapansi linanjenjemera ndi kuchita chivomerezi,

maziko a miyamba anagwedezeka;
ananjenjemera chifukwa Iye anakwiya.
9 M'mphuno mwake munatuluka utsi;
moto wonyeketsa unatuluka m'kamwa mwake,
makala amoto anali lawilawi m'kamwa mwake.
10 Iye anang'amba thambo natsika pansi;
pansi pa mapazi ake panali mitambo yakuda.
11 Iye anakwera pa Kerubi ndi kuwuluka;
nawuluka ndi mphepo mwaliwiro.
12 Iye anapanga mdima kukhala chofunda chake,
mitambo yakuda ya mlengalenga.
13 M'kuwala kumene kunali pamaso pake
munkachokera makala amoto alawilawi.
14 Yehova anabangula kumwamba ngati bingu,
mawu a Wammwambamwamba anamveka ponseponse.
15 Iye anaponya mivi yake, nabalalitsa adani ake,
ndi zing'aning'ani zake anawagonjetsa.
16 Zigwa za m'nyanja zinaonekera poyera,
ndipo maziko a dziko lapansi anakhala poyera,
Yehova atabangula mwaukali,
pamene mpweya wamphamvu unatuluka m'mphuno mwake.

17 "Ali kumwamba, Iye anatambalitsa dzanja lake ndipo anandigwira;
anandivuwula m'madzi ozama.
18 Anandipulumutsa kwa mdani wanga wamphamvu,
adani anga amene anali amphamvu kuposa ine.
19 Adaniwo analimbana nane pamene ndinali pa mavuto,
koma Yehova anali thandizo langa.
20 Iye anandipititsa kumalo otakasuka;
anandipulumutsa chifukwa amakondwera nane.

21 "Yehova wandithandiza molingana ndi chilungamo changa;
molingana ndi makhalidwe anga abwino, Iye wandipulumutsa.
22 Pakuti ine ndinatsata njira za Yehova;
ndilibe mlandu wochoka pamaso pa Mulungu wanga.
23 Malamulo ake onse ali pamaso panga,
sindinasiye malangizo ake.
24 Ndakhala moyo wosalakwa pamaso pake
ndipo ndakhala ndi kupewa tchimo.
25 Yehova wandipatsa mphotho molingana ndi chilungamo changa,
molingana ndi makhalidwe anga abwino pamaso pake.

26 "Kwa wokhulupirika, Inu mumaonetsa kukhulupirika kwanu,
kwa anthu amakhalidwe abwino, Inu mumaonetsanso makhalidwe abwino,
27 Kwa woyera mtima, Inu mumaonetsa kuyera mtima kwanu,
koma kwa anthu achinyengo mumaonetsanso kunyansidwa nawo.
28 Inu mumapulumutsa anthu odzichepetsa,
koma maso anu amatsutsana ndi odzikuza ndipo mumawatsitsa.
29 Inu Yehova, ndinu nyale yanga;
Yehova wasandutsa mdima wanga kukhala kuwunika.
30 Ndi thandizo lanu nditha kulimbana ndi gulu la ankhondo,

ndi Mulungu wanga nditha kuchita zosatheka ndi munthu.

31 “Kunena za Mulungu, zochita zake ndi zangwiro;
mawu a Yehova alibe cholakwika.
Iye ndi chishango
kwa onse amene amathawira kwa iye.
32 Mulungu wina ndi uti wofanana nanu Yehova?
Ndipo ndani amene ndi Thanthwe kupatula Mulungu wathu?
33 Ndi Mulungu amene anandipatsa mphamvu
ndi kulungamitsa njira yanga.
34 Iye amasandutsa mapazi anga kukhala ngati ambawala yayikazi;
Iye amandithandiza kuyimirira pamwamba pa mapiri.
35 Iye amaphunzitsa manja anga kuchita nkhondo;
manja anga amatha kuthyola uta wachitsulo.
36 Inu mundipatsa ine chishango chanu cha chigonjetso;
mumawerama kuti mundikweze.
37 Inu mwalimbitsa njira yanga kuti ndiyende bwino,
kuti mapazi anga asaterereke.

38 “Ine ndinathamangitsa adani anga ndi kuwakantha;
sindinabwerere mpaka iwo atawonongedwa.
39 Ndinawakantha kotheratu, ndipo sanathe kudzukanso;
Iwo anagwera pansi pa mapazi anga.
40 Inu munandipatsa ine mphamvu yochitira nkhondo;
munagwaditsa adani anga pa mapazi anga.
41 Inu muchititsa kuti adani anga atembenuke ndi kuthawa;
ndipo ndinawononga adani anga.
42 Iwo anafuwula kupempha thandizo, koma panalibe ndi mmodzi yemwe owapulumutsa.
Analirira kwa Yehova, koma sanawayankhe.
43 Ine ndinawaperesa ngati fumbi la pa dziko lapansi;
ndinawasinja ndipo ndinawapondaponda ngati matope a m’misewu.

44 “Inu mwandipulumutsa m’manja mwa mitundu ya anthu;
Inu mwandisunga kuti ndikhale mtsogoleri wa anthu a mitundu ina.
Anthu amene sindikuwadziwa ali pansi pa ulamuliro wanga.
45 Alendo amadzipereka okha pamaso panga;
akangomva za ine, amandigonjera.
46 Iwo onse anataya mtima;
anatuluka m’malinga awo akunjenjemera.

47 “Yehova ndi wamoyo! Litamandidwe Thanthwe langa.
Akuzike Mulungu, Thanthwe, Mpulumutsi wanga!
48 Iye ndi Mulungu amene amabwezera chilango,
amene amayika anthu a mitundu yonse pansi pa ulamuliro wanga,
49 amene amandimasula m’manja mwa adani anga.
Inu munandikuza kuposa adani anga;
munandilanditsa m’manja mwa anthu ankhanza.
50 Choncho ine ndidzakutamandani Inu Yehova, pakati pa anthu a mitundu ina;
ndidzayimba nyimbo zotamanda dzina lanu.

51 "Iye amapereka chipambano chachikulu kwa mfumu yake,
amaonetsa kukoma mtima kwa wodzozedwa wake,
kwa Davide ndi zidzukulu zake kwamuyaya."

# 23

*Mawu Otsiriza a Davide*

1 Nawa mawu otsiriza a Davide:
"Mawu a Davide mwana wa Yese,
mawu a munthu amene wakwezedwa ndi Wammwambamwamba,
munthu wodzozedwa ndi Mulungu wa Yakobo,
woyimba nyimbo za Israeli:

2 "Mzimu wa Yehova unayankhula kudzera mwa ine;
mawu ake anali pakamwa panga.
3 Mulungu wa Israeli anayankhula,
Thanthwe la Israeli linati kwa ine:
'Pamene munthu alamulira anthu mwachilungamo,
pamene alamulira moopa Mulungu,
4 amakhala ngati kuwala kwa mmamawa,
mmawa wopanda mitambo,
monga kuwala pamene mvula yaleka kugwa
imene imameretsa udzu m'nthaka.'

5 "Kodi banja langa silolungama pamaso pa Mulungu?
Kodi Iye sanachite pangano losatha ndi ine,
lokonzedwa ndi lotetezedwa mbali zonse?
Kodi sadzakwaniritsa chipulumutso changa,
ndi kundipatsa chokhumba changa chilichonse?
6 Koma anthu oyipa ndiwo ayenera kutayidwa kunja ngati minga,
imene sitengedwa ndi manja.
7 Aliyense amene wayikhudza mingayo
amayidula pogwiritsa ntchito chigwandali kapena ndodo ya mkondo;
nayitentha pa moto."

*Ankhondo Otchuka a Davide*

8 Nawa mayina a ankhondo amphamvu a Davide:

Yosebu-Basebeti wa ku Takemoni mkulu wa atsogoleri a ankhondo atatu. Iye anapha ndi mkondo ankhondo 800 nthawi imodzi.

9 Wotsatana naye anali Eliezara mwana wa Dodo Mwahohi. Monga
mmodzi mwa ankhondo atatu amphamvu a Davide, iye anali ndi
Davide pamene anazunza Afilisti amene anasonkhana ku Pasi-Damimu
kuchita nkhondo. Kenaka ankhondo a Israeli anabwerera m'mbuyo.
10 Koma iye anayima osasuntha ndipo anakantha Afilisti mpaka mkono
wake unatopa ndipo unakanirira ku lupanga lake. Yehova anapereka
chigonjetso chachikulu pa tsiku limenelo. Asilikali anabwerera kwa
Eliezara, kukatenga katundu wa anthu ophedwa.

11 Wotsatana naye anali Sama mwana wa Age Mharari. Pamene Afilisti
anasonkhana pamalo pamene panali munda wa mphodza, ankhondo a
Israeli anathawa Afilistiwo. 12 Koma Sama anayima pakati pa mundawo.
Iye anawuteteza nakantha Afilistiwo ndipo Yehova anawapambanitsa
koposa.

13 Pa nthawi yokolola, atatu mwa atsogoleri makumi atatu anabwera
kwa Davide ku phanga la Adulamu, pamene gulu la Afilisti linali litamanga
misasa m'chigwa cha Refaimu. 14 Nthawi imeneyo Davide anali mu
linga, ndipo boma la Afilisti linali ku Betelehemu. 15 Davide analakalaka
madzi ndipo anati, "Haa, pakanapezeka munthu wokanditungira madzi
a m'chitsime chomwe chili pafupi ndi chipata cha ku Betelehemu!"
16 Choncho anthu amphamvu atatuwa anadutsa mizere ya Afilisti, natunga
madzi amene anali m'chitsime chomwe chinali pafupi ndi chipata cha
ku Betelehemu nabwera nawo kwa Davide. Koma iye anakana kumwa.
M'malo mwake anathira pansi pamaso pa Yehova. 17 Iye anati, "Inu
Yehova, musalole kuti ine ndichite chinthu ichi! Kodi awa si magazi a
anthu amene anayika miyoyo yawo pachiswe?" Ndipo Davide sanamwe
madziwo.

Zimenezi ndi zimene anachita anthu amphamvu atatuwo.

18 Abisai m'bale wa Yowabu mwana wa Zeruya ndiye anali mtsogoleri
wa anthu atatuwa. Iye anapha ndi mkondo ankhondo 300, choncho
iyeyo anali wotchuka pakati pa anthu atatu aja. 19 Kodi iyeyo sanali
wolemekezeka koposa? Iye anakhala mtsogoleri wawo ngakhale kuti
sanali m'gulu la anthu atatu aja.

20 Benaya mwana wa Yehoyada wa ku Kabizeeli anali munthu wolimba
mtima amene anachita zinthu zamphamvu. Iye anakantha ankhondo
awiri otchuka a ku Mowabu. Tsiku lina kukuzizira kwambiri, iye analowa
m'dzenje ndi kuphamo mkango. 21 Ndipo iye anakanthanso Mwigupto
wamkulu msinkhu. Ngakhale kuti Mwiguptoyo anali ndi mkondo
m'dzanja mwake, Benaya anapita kukamenyana naye ali ndi chibonga
chokha m'manja. Iye analanda mkondo m'dzanja la Mwiguptoyo ndi
kumupha ndi mkondo wake womwe. 22 Izi ndi zamphamvu zimene
Benaya mwana wa Yehoyada anachita. Iyeyo analinso wotchuka ngati
anthu atatu amphamvu aja. 23 Iye ankalemekezedwa kuposa wina aliyense
mwa anthu makumi atatu aja, koma sanali m'gulu la anthu atatu aja.
Ndipo Davide anamuyika kukhala woyang'anira asilikali omuteteza.

24 M'gulu la anthu makumi atatu aja munalinso awa:
Asaheli m'bale wa Yowabu,
Elihanani mwana wa Dodo wa ku Betelehemu,
25 Sama Mharodi,
Elika Mherodi,
26 Helezi Mpaliti,
Ira mwana wa Ikesi wa ku Tekowa,
27 Abiezeri wa ku Anatoti,
Sibekai Mhusati,
28 Zalimoni Mwahohi,
Maharai Mnetofa,
29 Heledi mwana wa Baana Mnetofa,
Itai mwana wa Ribai wa ku Gibeya ku Benjamini,
30 Benaya Mpiratoni,
Hidayi wa ku zigwa za Gaasi.
31 Abi-Aliboni Mwaribati,
Azimaveti Mbarihumi,
32 Eliyahiba Msaaliboni,
ana a Yaseni,
Yonatani, 33 mwana wa Sama Mharari,

Ahiamu mwana wa Sarari Mharari,
34 Elifeleti mwana wa Ahasibai Mmaakati,
Eliamu mwana wa Ahitofele Mgiloni,
35 Heziro wa ku Karimeli,
Paarai Mwaribi,
36 Igala mwana wa Natani wa ku Zoba,
mwana wa Hagiri,
37 Zeleki Mwamoni,
Naharai wa ku Beeroti, mnyamata wonyamula zida za Yowabu mwana wa Zeruya,
38 Ira Mwitiri,
Garebu Mwitiri,
39 ndi Uriya Mhiti.

Onse pamodzi analipo 37.

# 24

*Davide Awerenga Ankhondo*

1 Nthawi inanso Yehova anawakwiyira Aisraeli ndipo anawutsa mtima wa Davide kuti awavutitse ndipo anati, “Pita kawerenge Aisraeli ndi Ayuda.”

2 Choncho mfumu inati kwa Yowabu pamodzi ndi atsogoleri a ankhondo amene anali nawo. “Pitani pakati pa mafuko onse a Israeli kuyambira ku Dani mpaka ku Beeriseba kuti mukawerenge anthu omenya nkhondo ndi cholinga choti ndidziwe chiwerengero chawo.”

3 Koma Yowabu anayankha mfumu kuti, “Yehova Mulungu wanu achulukitse ankhondo anu kukhala miyandamiyanda, ndipo alole inu mbuye wanga mfumu mudzazione zimenezi. Koma n’chifukwa chiyani inu mbuye wanga mfumu mukufuna kuchita zimenezi?”

4 Komabe mawu a mfumu anapambana mawu a Yowabu ndi atsogoleri a ankhondo. Choncho anachoka pamaso pa mfumu kupita kukawerenga anthu omenya nkhondo mu Israeli.

5 Atawoloka Yorodani, iwo anamanga misasa yawo pafupi ndi Aroeri
kummwera kwa mzinda wa ku chigwa ndipo kenaka iwo anapita ku
dziko la Gadi mpaka ku Yazeri.
6 Iwo anapita ku Giliyadi ndi ku chigwa
cha Tahitimu Hodisi ndipo anapitirira mpaka ku Dani Yaani ndi madera
ozungulira Sidoni.
7 Kenaka iwo anapita molunjika linga la ku Turo ndi
ku mizinda yonse ya Ahivi ndi Akanaani. Pomaliza anapita ku Beeriseba
ku Negevi wa ku Yuda.

8 Atayendayenda m’dziko lonse anabwerera ku Yerusalemu patapita miyezi isanu ndi inayi ndi masiku makumi awiri.

9 Yowabu anapereka chiwerengero cha anthu ankhondo kwa mfumu: Mu Israeli munali anthu 800,000 amphamvu amene amadziwa kugwiritsa ntchito lupanga ndipo mu Yuda munali anthu 500,000.

10 Davide anatsutsika mu mtima mwake atatha kuwerenga anthuwo ndipo anapemphera kwa Yehova kuti, “Ine ndachimwa kwambiri pa zimene ndachita. Tsono Yehova, ndikupempha kuti mukhululuke kulakwa kwa mtumiki wanu. Ine ndachita zopusa kwambiri.”

11 Davide asanadzuke mmawa mwake mawu a Yehova anafika kwa
mneneri Gadi, mlosi wa Davide kuti,
12 “Pita ukamuwuze Davide kuti,
‘Yehova akuti, Ine ndikukupatsa zinthu zitatu izi. Usankhepo chimodzi
pa zimenezi choti ndikuchitire.’ ”

13 Choncho Gadi anapita kwa Davide ndipo anati kwa iye, “Kodi
mungakonde kuti m’dziko mwanu mukhale njala kwa zaka zitatu? Kapena
kuti mukhale mukuthawa adani anu kwa miyezi itatu? Kapena kuti
m’dziko muno mukhale mliri kwa masiku atatu? Tsopano, ganizirani
bwino ndipo musankhe chomwe mudzamuyankhe amene wandituma.”
14 Davide anati kwa Gadi, “Ine ndavutika kwambiri mu mtima mwanga.
Ife atilange ndi Yehova pakuti chifundo chake ndi chachikulu, koma
ndisalangidwe ndi anthu.”
15 Choncho Yehova anabweretsa mliri pa Aisraeli, kuyambira mmawa
mpaka pa nthawi imene anafuna mwini wake, ndipo unapha anthu 70,000
kuyambira ku Dani mpaka ku Beeriseba. 16 Pamene mngelo anatambasula
dzanja lake kuti awononge Yerusalemu, Yehova anamva chisoni chifukwa
cha zowawazo ndipo anati kwa mngelo amene ankawononga anthu uja,
“Basi kwakwanira! Leka kuwononga.” Nthawi imeneyo mngelo wa
Yehova anali atayima pamalo opunthira tirigu a Arauna Myebusi.
17 Davide ataona mngelo amene ankakantha anthu uja, anati kwa
Yehova, “Ine ndi amene ndachimwa. Ine m’busa ndiye ndachita zoyipa.
Anthuwa ali ngati nkhosa zosalakwa. Kodi iwowa achita chiyani? Langani
ineyo pamodzi ndi banja langa.”

### *Davide Amanga Guwa la Nsembe*

18 Tsiku limenelo Gadi anapita kwa Davide ndi kukanena kuti, “Pitani
kamangeni guwa lansembe la Yehova pamalo opunthira tirigu a Arauna
Myebusi.” 19 Ndipo Davide anapita monga momwe Yehova anamulamulira
kudzera mwa Gadi. 20 Arauna atayang’ana ndi kuona mfumu ndi anthu
ake akubwera kumene kunali iye, iyeyo anatuluka ndi kuwerama pamaso
pa mfumu mpaka nkhope yake kugunda pansi.
21 Arauna anati, “N’chifukwa chiyani mbuye wanga mfumu mwabwera
kwa mtumiki wanu?”
Davide anayankha kuti, “Kudzagula malo ako opunthira tirigu kuti
ndimangire Yehova guwa lansembe kuti mliri uli pa anthuwa usiye.”
22 Arauna anati kwa Davide, “Mbuye wanga mfumu mutenge chili-
chonse chimene chikukondweretseni ndi kuchipereka nsembe. Nazi
ng’ombe zazimuna za nsembe yopsereza, nazi zopunthira tirigu ndi
magoli ang’ombe kuti zikhale nkhuni. 23 Inu mfumu, Arauna akupereka
zonsezi kwa inu mfumu.” Arauna anatinso kwa iye, “Yehova Mulungu
wanu akuvomerezeni.”
24 Koma mfumu inayankha Arauna kuti, “Ayi, Ine ndikunenetsa
kuti ndikulipira. Sindidzapereka kwa Yehova Mulungu wanga nsembe
yopsereza imene sindinavutikire.”
Kotero Davide anagula malo wopunthira tiriguwo ndi ng’ombe ndipo
anapereka kwa Araunayo masekeli asiliva makumi asanu. 25 Davide
anamanga guwa lansembe la Yehova pamenepo ndipo anaperekapo
nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano. Ndipo Yehova anayankha
pempherolo m’malo mwa dziko lonse, ndipo mliri unatha pa Aisraeli.

# 1 Mafumu

### *Adoniya Adziyika Kukhala Mfumu*

1 Mfumu Davide atakalamba sankamva kufunda ngakhale akamufun-
ditsa mabulangeti. 2 Choncho nduna zake zinamuwuza kuti, “Tiloleni
tifune namwali woti azikhala nanu ndi kumakusamalirani. Namwaliyo
azigona pafupi nanu kuti mbuye wathu mfumu muzimva kufundira.”
3 Kotero anafunafuna m’dziko lonse la Israeli mtsikana wokongola
ndipo anapeza Abisagi wa ku Sunemu, nabwera naye kwa mfumu.
4 Mtsikanayo anali wokongola kwambiri ndipo ankasamalira mfumu ndi
kumayitumikira, koma mfumuyo sinakhale naye malo amodzi.
5 Nthawi imeneyi Adoniya, mwana wa Hagiti, anayamba kudzitukumula
ndipo anati, “Ndidzakhala mfumu ndine.” Choncho anadzikonzera galeta
ndi akavalo, pamodzi ndi anthu 50 woti azithamanga patsogolo pake.
6 (Abambo ake sanalowererepo n’kamodzi komwe ndipo sanafunsepo kuti,
“N’chifukwa chiyani ukuchita zimenezi?” Adoniyayo anali wokongola
kwambiri ndipo anali wopondana ndi Abisalomu).
7 Adoniya anagwirizana ndi Yowabu mwana wa Zeruya ndiponso
Abiatara wansembe, ndipo iwowa anamuthandiza. 8 Koma Zadoki
wansembe, Benaya mwana wa Yehoyada, mneneri Natani, Simei ndi Rei
ndiponso asilikali amphamvu a Davide sanamutsate Adoniya uja.
9 Kenaka Adoniya anapereka nsembe za nkhosa ndi ng’ombe ndiponso
ana ang’ombe onenepa ku Mwala wa Zohereti kufupi ndi Eni Rogeli. Iye
anayitana abale ake onse, ana aamuna a mfumu ndiponso akuluakulu
onse a ku Yuda, 10 koma sanayitane mneneri Natani kapena Benaya
kapenanso asilikali amphamvu a Davide ngakhalenso m’bale wake
Solomoni.
11 Pamenepo Natani anafunsa Batiseba, amayi ake a Solomoni, kuti,
“Kodi simunamve kuti Adoniya, mwana wa Hagiti, walowa ufumu
popanda Davide mbuye wathu kudziwa? 12 Tsopano ine ndikulangizeni
inu mmene mungapulumutsire moyo wanu ndi moyo wa mwana wanu
Solomoni. 13 Pitani msanga kwa Mfumu Davide ndipo mukanene kuti,
‘Mbuye wanga mfumu, kodi simunalumbire kwa ine mdzakazi wanu kuti,
‘Ndithu mwana wako Solomoni ndiye adzakhale mfumu m’malo mwanga,
ndipo adzakhala pa mpando wanga waufumu?’ Nanga n’chifukwa chiyani
Adoniya walowa ufumu?’ 14 Pamene inu muzikayankhula ndi mfumu, ine
ndidzalowa ndi kuchitira umboni mawu anuwo.”
15 Choncho Batiseba anapita nakalowa ku chipinda kukaonana ndi
mfumu imene inali itakalamba kwambiri, kumene Abisagi wa ku Sunemu
uja ankayisamalira. 16 Batiseba anagwada nalambira mfumu.
Mfumu inamufunsa kuti, “Kodi n’chiyani chimene ukufuna?”
17 Iye anayankha kuti, “Mbuye wanga, inu mwini munalumbira kwa
ine mdzakazi wanu m’dzina la Yehova Mulungu wanu kuti, ‘Solomoni
mwana wako ndiye adzakhale mfumu m’malo mwa ine, ndipo adzakhala
pa mpando wanga waufumu.’ 18 Koma tsopano Adoniya ndiye walowa
ufumu, ndipo inu mbuye wanga mfumu, simukuzidziwa zimenezi.
19 Ndipo wapereka nsembe ng’ombe zambiri, ana ang’ombe onenepa ndi
nkhosa ndi mbuzi ndipo wayitana ana anu onse, wansembe Abiatara

ndiponso Yowabu mkulu wa ankhondo, koma sanayitane kapolo wanu
Solomoni. 20 Mbuye wanga mfumu, maso a Aisraeli onse ali pa inu,
kuti adziwe kuchokera kwa inu amene adzakhala pa mpando waufumu
wa mbuye wanga m'malo mwanu. 21 Mukapanda kutero, mbuye
wanga, mukadzangotisiya n'kulondola kumene kunapita makolo anu, ine
pamodzi ndi mwana wangayu Solomoni adzatiyesa owukira."

22 Pamene Batiseba amayankhula ndi mfumu, mneneri Natani analowa.
23 Ndipo anthu anawuza mfumu kuti, "Kwabwera mneneri Natani."
Kotero iye anafika pamaso pa mfumu ndipo anawerama nagunditsa
nkhope yake pansi.

24 Natani anafunsa kuti, "Mbuye wanga mfumu, kodi mwalengeza
kuti Adoniya adzakhala mfumu m'malo mwanu, ndi kuti adzakhala
pa mpando wanu waufumu? 25 Lero lomwe lino wakapereka nsembe
ng'ombe zambiri, ana ang'ombe onenepa ndiponso nkhosa ndi mbuzi.
Iye wayitana ana anu onse, atsogoleri a nkhondo, ndiponso wansembe
Abiatara. Panopa onsewa akudya ndi kumwa naye ndipo akunena kuti,
'Akhale ndi moyo wautali mfumu Adoniya!' 26 Koma ine kapolo wanu,
wansembe Zadoki ndi Benaya mwana wa Yehoyada, ndiponso kapolo
wanu Solomoni sanatiyitane. 27 Kodi zimenezi mbuye wanga mfumu
mwazichita ndinu, osawawuza atumiki anu kuti adziwe amene adzakhale
pa mpando waufumu m'malo mwanu?"

### *Davide Alonga Ufumu Solomoni*

28 Pamenepo mfumu Davide anati, "Muyitaneni Batiseba." Kotero
Batiseba analowa ndipo anayimirira pamaso pa mfumu.

29 Tsono mfumu inalumbira kuti, "Pali Yehova wamoyo, amene
anandipulumutsa ine ku mavuto onse, 30 ndithu ine lero ndichita zonse
zimene ndinalumbira kwa Yehova Mulungu wa Israeli kuti, mwana wako
Solomoni adzakhala mfumu m'malo mwanga ndipo adzakhala pa mpando
wanga waufumu."

31 Pamenepo Batiseba anawerama, nagunditsa mutu wake pansi nalam-
bira mfumu, ndipo anati, "Mbuye wanga Mfumu Davide mukhale ndi
moyo wautali!"

32 Mfumu Davide anati, "Ndiyitanireni wansembe Zadoki, mneneri
Natani ndi Benaya mwana wa Yehoyada." Atafika pamaso pa mfumu,
33 mfumuyo inati kwa iwo, "Tengani atumiki anga ndipo mukweze mwana
wanga Solomoni pa bulu wanga ndipo mupite naye ku Gihoni. Mukalize
lipenga ndi kufuwula kuti, 'Akhale ndi moyo wautali mfumu Solomoni!'
34 Kumeneko Zadoki wansembe ndi mneneri Natani akamudzoze kuti
akhale mfumu ya Israeli. Kenaka mukalize lipenga ndi kumanena kuti
'Akhale ndi moyo wautali Mfumu Solomoni.' 35 Ndipo pobwera muzika-
mutsata pambuyo. Iyeyo akabwere kuno ndi kudzakhala pa mpando
wanga waufumu ndi kudzalamulira m'malo mwanga. Ndamusankha
kukhala wolamulira Israeli ndi Yuda."

36 Benaya mwana wa Yehoyada anayankha mfumu kuti, "Ameni! Yehova
Mulungu wa mbuye wanga mfumu akhazikitse kuti zichitike motero.
37 Monga momwe Yehova wakhalira ndi inu mbuye wanga mfumu,
momwemonso akhale ndi Solomoni ndi kukhazikitsa ufumu wake kuti
ukhale waukulu kuposa ufumu wa mbuye wanga Mfumu Davide!"

38 Kotero Zadoki wansembe, mneneri Natani, Benaya mwana wa
Yehoyada, Akereti ndiponso Apeleti, anthu oteteza mfumu, anapita

kukamukweza Solomoni pa bulu wa Mfumu Davide ndi kupita naye ku
Gihoni. 39 Wansembe Zadoki anatenga nyanga ya mafuta yochokera ku
malo opatulika ndi kumudzoza Solomoni. Kenaka analiza lipenga ndipo
anthu onse anafuwula kuti, "Akhale ndi moyo wautali Mfumu Solomoni!"
40 Ndipo anthu onsewo anapita namutsatira pambuyo akuyimba zitoliro
ndi kukondwerera kwambiri, kotero nthaka inagwedezeka chifukwa cha
phokoso lawo.

41 Adoniya pamodzi ndi anthu onse oyitanidwa amene anali naye
anamva zimenezi pamene ankamaliza madyerero awo. Atamva kulira
kwa malipenga, Yowabu anafunsa kuti, "Kodi phokoso lonselo mu
mzindamo likutanthauza chiyani?"

42 Iye akuyankhula, Yonatani mwana wa wansembe Abiatara anafika.
Adoniya anati, "Lowa. Munthu wabwino ngati iwe ayenera kubweretsa
nkhani yabwino."

43 Yonatani anayankha Adoniya kuti, "Ayi ndithu, zinthu sizili bwino!
Mbuye wathu Mfumu Davide walonga Solomoni ufumu. 44 Mfumu yatuma
Zadoki wansembe, mneneri Natani, Benaya mwana wa Yehoyada, Akereti
ndi Apeleti ku Gihoni ndipo iwo amukweza pa bulu wa mfumu, 45 ndipo
Zadoki wansembe ndi mneneri Natani adzoza Solomoni ku Gihoni kuti
akhale mfumu. Ndipo kuchokera kumeneko akhala akululutira, kotero
kuti mu mzinda monse muli phokoso lokhalokha. Ndiyetu phokoso
limene mukulimvalo. 46 Ndipo Solomoni wakhala kale pa mpando wake
waufumu. 47 Kuwonjezera pamenepo, nduna za mfumu zabwera kale
kudzayamika mbuye wathu Mfumu Davide, pomanena kuti, 'Mulungu
wanu atchukitse dzina la Solomoni kuposa dzina lanu ndipo ufumu wake
ukule kupambana ufumu wanu!' Ndipo mfumu inawerama niyamba
kupembedza pa bedi lake, 48 inati, 'Atamandike Yehova, Mulungu wa
Israeli, amene wasankha wolowa m'malo mwanga ine ndikanali ndi moyo
lero lino.' "

49 Anthu onse amene Adoniya anawayitana ananjenjemera ndi mantha,
ndipo anayimirira, kenaka anamwazikana. 50 Koma Adoniya, poopa
Solomoni, anapita ku Nyumba ya Mulungu nakagwira msonga za guwa
lansembe. 51 Tsono Solomoni anawuzidwa kuti, "Adoniya akukuopani inu
Mfumu Solomoni ndipo wagwira msonga za guwa lansembe. Iye akuti,
'Mfumu Solomoni alumbire kuti sadzapha kapolo wake ndi lupanga.' "

52 Solomoni anayankha kuti, "Ngati iyeyo aonetse kuti ndi munthu
wakhalidwe labwino, ngakhale tsitsi la m'mutu mwake silidzathothoka
ndi kugwera pansi, koma akapezeka kuti ali ndi khalidwe loyipa,
adzafa ndithu." 53 Pamenepo Mfumu Solomoni inatuma anthu ndipo
anakamutenga paguwa paja. Adoniya anabwera ndi kudzalambira Mfumu
Solomoni, ndipo Solomoni anati, "Pita ku nyumba yako."

# 2

### *Davide Alangiza Solomoni*

1 Davide ali pafupi kumwalira, analangiza mwana wake Solomoni kuti:
2 "Ndatsala pang'ono kupita kumene munthu wina aliyense amayen-
era kupitako. Tsono khala wamphamvu, uvale zilimbe, 3 ndipo uzi-
chita zimene Yehova Mulungu wako amafuna, uziyenda m'njira zake,
uzisunga malangizo ndi malamulo ake monga momwe zinalembedw-
era m'Malamulo a Mose, kuti zonse zimene udzachite zidzakuyendere

bwino kulikonse kumene udzapite. 4 Ndipo Yehova akwaniritse zimene
anandilonjeza kuti, 'Ngati zidzukulu zako zidzakhala mosamala, niziyenda
mokhulupirika pamaso panga ndi mtima wawo wonse ndi moyo wawo
wonse, sudzasowa munthu wokhala pa mpando waufumu wa Israeli.'

5 "Tsono iwe ukudziwanso zoyipa zimene Yowabu mwana wa Zeruya
anandichitira pakupha atsogoleri awiri a ankhondo a Israeli, Abineri
mwana wa Neri ndi Amasa mwana wa Yeteri. Iye anawapha ndi kukhetsa
magazi nthawi ya mtendere ngati nthawi ya nkhondo, ndipo anapaka
magazi amenewo pa lamba wa m'chiwuno mwake ndi pa nsapato za ku
mapazi ake. 6 Iwe uchite kwa iye molingana ndi nzeru zako, koma usalole
kuti afe ndi ukalamba ndi kupita ku manda mwamtendere.

7 "Koma ana a Barizilai wa ku Giliyadi uwakomere mtima ndipo
uwalole kuti akhale m'gulu la anthu amene azidya pamodzi nawe. Pakuti
anandisamalira pamene ndinkathawa m'bale wako Abisalomu.

8 "Ndipo kumbukira kuti uli ndi Simei mwana wa Gera, wa fuko la
Benjamini wochokera ku Bahurimu, amene ananditemberera koopsa tsiku
limene ndimapita ku Mahanaimu. Atabwera kudzakumana nane ku
Yorodani, ine ndinalumbira m'dzina la Yehova kuti, 'Sindidzakupha iwe
ndi lupanga.' 9 Koma tsopano usamuyese ngati munthu wosalakwa. Iwe
ndiwe munthu wanzeru. Udzadziwa choti uchite naye. Ngakhale ndi
wokalamba, aphedwe ndithu."

10 Tsono Davide anamwalira ndipo anayikidwa m'manda mu Mzinda
wa Davide. 11 Iyeyo n'kuti atalamulira Israeli kwa zaka makumi anayi.
Ku Hebroni analamulira zaka zisanu ndi ziwiri ndipo ku Yerusalemu
analamulira zaka 33. 12 Choncho Solomoni anakhala pa mpando waufumu
wa abambo ake Davide, ndipo ufumu wake unakhazikika kwambiri.

### *Kukhazikika kwa Ufumu wa Solomoni*

13 Tsono Adoniya, mwana wa Hagiti, anapita kwa Batiseba, amayi ake a
Solomoni. Batiseba anamufunsa kuti, "Kodi wabwera mwamtendere?"

Iye anayakha kuti, "Eya, ndi zamtendere." 14 Ndipo iye anawonjezera
kunena kuti, "Ndili ndi mawu oti ndiyankhule nanu."

Batiseba anayankha kuti, "Yankhula."

15 Tsono Adoniya anati, "Monga inu mukudziwa, ufumu unali wanga.
Aisraeli onse ankayembekezera kuti ine ndidzakhala mfumu yawo. Koma
zinthu zinasintha ndipo ufumu wapita kwa m'bale wanga; pakuti wapatsa
iye ufumuwu ndi Yehova. 16 Tsono ndili ndi pempho limodzi kwa inu.
Musandikanize ayi."

Batiseba anati, "Nena."

17 Adoniya anapitiriza kunena kuti, "Chonde, inu mupemphe mfumu
Solomoni kuti andipatse Abisagi wa ku Sunemu kuti akhale mkazi wanga
pakuti mukapempha inu sadzakukanizani."

18 Batiseba anayankha kuti, "Chabwino. Ndidzakuyankhulira kwa
mfumu."

19 Batiseba atapita kwa Mfumu Solomoni kukayankhula naye m'malo
mwa Adoniya, mfumu inanyamuka kukumana naye, ndipo inaweramira
amayi akewo, kenaka inakhala pa mpando wake waufumu. Iye anayi-
tanitsa mpando wina kuti amayi ake akhalepo ndipo anakhala pansi ku
dzanja lake lamanja.

20 Amayi akewo anati, "Ndikufuna ndikupempheni kanthu kakang'ono.
Chonde musandikanize."

Mfumu inayankha kuti, "Pemphani amayi, ine sindikukanizani."

21 Ndipo amayiwo anati, “Mulole kuti Abisagi wa ku Sunemu akhale
mkazi wa m’bale wanu Adoniya.”

22 Koma Mfumu Solomoni inayankha amayi ake aja kuti, “Chifukwa
chiyani mukupemphera Adoniya Abisagi wa ku Sunemu? Mungathenso
kumupemphera ufumu pakuti iyeyu ndi mkulu wanga ndipo mupem-
phereninso wansembe Abiatara ndi Yowabu mwana wa Zeruya!”

23 Pamenepo Mfumu Solomoni inalumbira m’dzina la Yehova kuti,
“Mulungu andilange ine koopsa ngati Adoniya saphedwa chifukwa cha
pempho lakeli! 24 Tsono pali Yehova wamoyo, amene anandikhazikitsa
ine pa mpando waufumu wa abambo anga Davide ndi kundipatsa ufumu
monga analonjezera, Adoniya aphedwa lero lomwe lino!” 25 Choncho
Mfumu Solomoni inalamula Benaya mwana wa Yehoyada ndipo anakan-
tha Adoniyayo, nafa.

26 Ndipo mfumu inati kwa Abiatara wansembe, “Pita ku Anatoti ku
minda yako chifukwa ndiwe woyenera kufa, koma sindikupha tsopano,
chifukwa unkanyamula Bokosi la Chipangano la Ambuye Yehova pamaso
pa abambo anga Davide ndipo unazunzika limodzi ndi abambo angawo.”
27 Kotero Solomoni anachotsa Abiatara pa udindo wokhala wansembe wa
Yehova, kukwaniritsa mawu a Yehova amene anayankhula za nyumba ya
Eli ku Silo.

28 Yowabu atamva zimenezi anathawira ku tenti ya Yehova ndipo anak-
agwira msonga za guwa lansembe, popeza Yowabu ndiye anathandiza
Adoniya kuwukira koma sanathandize Abisalomu. 29 Mfumu Solomoni
inawuzidwa kuti Yowabu wathawira ku tenti ya Yehova ndipo ali pambali
pa guwa lansembe. Tsono Solomoni analamula Benaya mwana wa
Yehoyada kuti, “Pita, kamukanthe!”

30 Choncho Benaya analowa m’tenti ya Yehova ndipo anati kwa Yowabu,
“Mfumu ikuti ‘Tuluka!’ ”

Koma iye anayankha kuti, “Ayi, ine ndifera muno.”

Benaya anakafotokozera mfumu kuti, “Umu ndi mmene Yowabu
wandiyankhira.”

31 Pamenepo mfumu inalamula Benaya kuti, “Kachite monga iye wanen-
era. Ukamukanthe ndi kumuyika m’manda. Ukatero udzandichotsera ine
pamodzi ndi nyumba ya abambo anga mlandu wa anthu osalakwa amene
Yowabu anawapha. 32 Yehova adzamubwezera zomwe anachita pokhetsa
magazi, chifukwa iye anakantha ndi lupanga anthu awiri abwino ndi
olungama kuposa iye, nawapha, abambo anga Davide osadziwa. Anthu
awiriwo ndi Abineri mwana wa Neri, wolamulira gulu lankhondo la
Israeli ndi Amasa mwana wa Yeteri, wolamulira gulu lankhondo la Yuda.
33 Magazi amene Yowabu anakhetsa akhale pamutu pake ndi pa zidzukulu
zake kwamuyaya. Koma pa Davide ndi zidzukulu zake, nyumba yake
ndi mpando wake waufumu pakhale mtendere wochokera kwa Yehova
kwamuyaya.”

34 Choncho Benaya mwana wa Yehoyada anapita kukakantha Yowabu
n’kumupha ndipo anayikidwa m’manda m’nyumba yakeyake ya ku
chipululu. 35 Mfumu inayika Benaya mwana wa Yehoyada kuti akhale
woyang’anira gulu lankhondo m’malo mwa Yowabu ndipo inayika Zadoki
kuti akhale wansembe m’malo mwa Abiatara.

36 Kenaka mfumu inatuma anthu kukayitana Simei ndipo inamuwuza
kuti, “Udzimangire nyumba mu Yerusalemu ndipo uzikhala kumeneko,
koma usatuluke mu mzinda kupita kwina kulikonse. 37 Tsiku lomwe

udzatulukemo ndi kuwoloka Chigwa cha Kidroni, udziwiretu kuti udzafa ndipo magazi ako adzakhala pamutu pako."

38 Simei anayankha mfumu kuti, "Zimene mwanenazi n'zabwino. Kapolo wanu adzachita monga mbuye wanga mfumu mwanenera." Choncho Simei anakhala mu Yerusalemu nthawi yayitali.

39 Koma patatha zaka zitatu, akapolo awiri a Simei anathawira kwa Akisi mwana wa Maaka, mfumu ya ku Gati, ndipo Simei anawuzidwa kuti,
"Akapolo anu ali ku Gati."
40 Atamva zimenezi, anakwera bulu wake ndipo anapita kwa Akisi ku Gati kukafunafuna akapolo ake. Choncho Simei anapita ndi kukatenga akapolo ake ku Gati ndipo anabwera nawo.

41 Solomoni atawuzidwa kuti Simei anatuluka mu Yerusalemu ndi
kupita ku Gati ndipo kuti wabwerako,
42 mfumu inamuyitanitsa Simei ndipo inamufunsa kuti, "Kodi sindinakulumbiritse m'dzina la Yehova ndi kukuchenjeza kuti, 'Tsiku limene udzatuluka kupita kwina kulikonse, udziwe kuti udzafa'? Nthawi imeneyo iwe unandiwuza kuti, 'Zimene
mwanena n'zabwino. Ine ndidzamvera.'
43 Chifukwa chiyani tsono sunasunge lumbiro lako kwa Yehova? Bwanji nanga sunamvere lamulo limene ndinakuwuza?"

44 Mfumuyo inawuzanso Simei kuti, "Ukudziwa mu mtima mwakomo zoyipa zonse zimene unachitira abambo anga Davide. Tsopano Yehova
akubwezera zoyipa zakozo.
45 Koma Mfumu Solomoni idzadalitsidwa ndipo mpando waufumu wa Davide udzakhazikika pamaso pa Yehova kwamuyaya."

46 Pamenepo mfumu inalamula Benaya mwana wa Yehoyada ndipo iye anapita kukakantha Simei ndi kumupha.

Tsono ufumu unakhazikika m'dzanja la Solomoni.

# 3

*Solomoni Apempha Nzeru*

1 Solomoni anachita ubale ndi Farao mfumu ya ku Igupto ndipo anakwatira mwana wake wamkazi. Mkaziyo anabwera naye mu Mzinda wa Davide mpaka anatsiriza kumanga nyumba yaufumu ndi Nyumba
ya Yehova ndiponso khoma lozungulira Yerusalemu.
2 Koma anthu ankaperekabe nsembe ku malo achipembedzo osiyanasiyana chifukwa chakuti mpaka pa nthawi imeneyo Dzina la Yehova anali asanalimangire
nyumba.
3 Solomoni anaonetsa chikondi chake pa Yehova poyenda motsatira malamulo a abambo ake Davide, kupatula kuti ankapereka nsembe ndi kufukiza lubani ku malo osiyanasiyana achipembedzo.

4 Mfumu inapita ku Gibiyoni kukapereka nsembe popeza kumeneko ndiye kunali malo oposa malo ofunika kwambiri pachipembedzo. Kumeneko Solomoni anapereka nsembe zopsereza 1,000 pa guwa
lansembe.
5 Ku Gibiyoniko Yehova anaonekera kwa Solomoni m'maloto usiku, ndipo Mulungu anati, "Pempha chilichonse chimene ukufuna ndipo ndidzakupatsa."

6 Solomoni anayankha kuti, "Inu munaonetsa kukoma mtima kwanu kwakukulu kwa kapolo wanu, abambo anga Davide, chifukwa anali wokhulupirika pamaso panu, wolungama mtima ndiponso wa mtima wangwiro. Inu mukupitirizabe kukoma mtima kwanu kwakukulu kwa iye ndipo mwamupatsa mwana kuti akhale pa mpando wake waufumu lero lino.

7 “Tsopano Inu Yehova Mulungu wanga, mtumiki wanune mwandiyika
kukhala mfumu m’malo mwa abambo anga Davide. Komatu ndine
mwana wamng’ono ndipo sindidziwa kagwiridwe kake ka ntchito yangayi.
8 Mtumiki wanu ali pakati pa anthu amene munawasankha, mtundu
waukulu, anthu ochuluka kwambiri osatheka kuwawerenga. 9 Choncho
mupatseni mtumiki wanu nzeru zolamulira anthu anu ndi kuti azitha
kusiyanitsa pakati pa chabwino ndi choyipa. Pakuti ndani amene angathe
kulamulira anthu anu ochulukawa?”

10 Ambuye anakondwera kuti Solomoni anapempha zimenezi. 11 Tsono
Mulungu anati kwa Solomoni, “Popeza wapempha zinthu zimenezi osati
moyo wautali kapena chuma chako kapena imfa ya adani ako koma
nzeru zolamulira anthu mwachilungamo, 12 Ine ndidzakuchitira zimene
wapempha. Ndidzakupatsa mtima wanzeru ndi wozindikira zinthu,
kotero kuti sipanakhalepo wina wofanana nawe ndipo sipadzapezekanso
wina wonga iwe pambuyo pako. 13 Kuwonjeza apo, ndidzakupatsa zimene
sunazipemphe: chuma ndi ulemu, kotero kuti pa masiku onse a moyo
wako sipadzakhala mfumu yofanana nawe. 14 Ndipo ngati udzayenda
m’njira zanga ndi kumvera malamulo anga ndiponso malangizo anga
monga abambo ako Davide anachitira, ndidzakupatsa moyo wautali.”
15 Kotero Solomoni anadzuka ndipo anazindikira kuti anali maloto.

Iye anabwerera ku Yerusalemu nakayimirira patsogolo pa Bokosi la
Chipangano la Ambuye ndipo anapereka nsembe zopsereza ndi nsembe
zachiyanjano. Kenaka anakonzera phwando atumiki ake onse.

### *Kuweruza Kolungama*

16 Nthawi ina amayi awiri adama anabwera kwa mfumu ndipo anayima
pamaso pake. 17 Mmodzi mwa amayiwo anati, “Mbuye wanga, mayi uyu
ndi ine timakhala nyumba imodzi. Ine ndinabala mwana tili limodzi ndi
mnzangayu. 18 Tsiku lachitatu ine nditabala mwana, mnzangayunso an-
abereka mwana wake. Tinalipo awiriwiri m’nyumbamo ndipo munalibe
wina aliyense.

19 “Nthawi ya usiku mwana wa mnzangayu anafa chifukwa anamu-
gonera. 20 Tsono iyeyu anadzuka pakati pa usiku, natenga mwana wanga
ku mimba kwanga pamene ine mdzakazi wanu ndinali m’tulo. Ana-
muyika mwanayo ku mimba kwake ndi kuyika mwana wake wakufayo
ku mimba kwanga. 21 Mmawa nditadzuka kuti ndiyamwitse mwana
wanga ndinapeza kuti ndi wakufa! Koma kutacha nditamuyang’anitsitsa
ndinaona kuti si mwana amene ine ndinabala.”

22 Koma mayi winayo anati, “Ayi! Mwana wamoyoyu ndi wanga, mwana
wakufayu ndi wako.”

Koma mayi woyambayo analimbikira kuti. “Ayi! Mwana wakufayu ndi
wako; wamoyoyu ndi wanga.” Motero akaziwa anatsutsana pamaso pa
mfumu.

23 Pamenepo mfumu inati, “Wina akuti, ‘Mwana wanga ndi wamoyoyu
ndipo mwana wako ndi wakufayu,’ pamene winanso akuti, ‘Ayi! Mwana
wako ndi wakufayu wanga ndi wamoyoyu.’ ”

24 Pamenepo mfumu inati, “Patseni lupanga.” Ndipo anabwera nalo
lupanga kwa mfumu. 25 Tsono mfumu inagamula kuti, “Muduleni pakati
mwana wamoyoyu ndipo wina mumupatse gawo limodzi, gawo linalo
mumupatse winayo.”

26 Mayi amene mwana wake anali moyo anagwidwa ndi chisoni chifukwa cha mwana wakeyo ndipo anawuza mfumu kuti, “Chonde mbuye wanga, mupatseni mnzangayu mwana wamoyoyu! Musamuphe!”
Koma winayo anati, “Ayi, asandipatse ine kapena iwe. Muduleni pakati!”
27 Choncho mfumu inagamula kuti, “Perekani mwana wamoyoyu kwa mayi woyambayu. Musamuphe, iyeyu ndiye mayi wake wa mwanayu.”
28 Pamene Aisraeli onse anamva za chigamulo chimene mfumu inapereka, anaopa mfumuyo kwambiri, chifukwa anaona kuti mfumu inali ndi nzeru zochokera kwa Mulungu zoweruzira mwachilungamo.

# 4

*Nduna za Solomoni ndi Abwanamkubwa*

1 Ndipo Mfumu Solomoni inakhala mfumu ya Aisraeli onse.
2 Nduna zake zikuluzikulu zinali izi:

Azariya mwana wa Zadoki anali wansembe;
3 Elihorefe ndi Ahiya, ana a Sisa, anali alembi;
Yehosafati mwana wa Ahiludi, anali mlembi wa zochitika;
4 Benaya mwana wa Yehoyada, anali mtsogoleri wa ankhondo;
Zadoki ndi Abiatara, anali ansembe;
5 Azariya mwana wa Natani, anali woyang’anira nduna za m’zigawo;
Zabudi mwana wa Natani, anali wansembe ndi bwenzi la mfumu;
6 Ahisara, anali mkulu woyang’anira nyumba ya mfumu;
Adoniramu mwana wa Abida, anali mkulu woyang’anira ntchito za thangata.

7 Solomoni analinso ndi abwanamkubwa khumi ndi awiri amene ankayang’anira zigawo zonse za dziko la Israeli. Iwo ankapereka chakudya kwa mfumu ndiponso ku banja laufumu. Bwanamkubwa aliyense ankapereka chakudya mwezi umodzi pa chaka.
8 Mayina awo ndi awa:

Beni-Huri, wa ku dziko la mapiri la Efereimu;
9 Beni-Dekeri, woyang’anira mizinda ya Makazi, Saalibimu, Beti-Semesi ndi Eloni Beti-Hanani;
10 Beni-Hesedi, woyang’anira mizinda ya Aruboti (Soko ndi dziko lonse la Heferi);
11 Beni-Abinadabu, woyang’anira Nafoti Dori (iye anakwatira Tafati mwana wa Solomoni);
12 Baana mwana wa Ahiludi, anali woyang’anira Taanaki ndi Megido, ndi ku Beti Sani konse, kufupi ndi ku Zaretani kumunsi kwa Yezireeli, kuyambira ku Beti-Seani mpaka ku Abeli-Mehola kukafika mpaka ku Yokineamu;
13 Beni-Geberi, anali woyang’anira Ramoti Giliyadi (midzi ya Yairi inali ya mwana wa Manase ku Giliyadi, pamodzinso ndi chigawo cha Arigobu ku Basani ndiponso mizinda yake yayikulu makumi asanu ndi umodzi yokhala ndi malinga ndi mipiringidzo yamkuwa).
14 Ahinadabu mwana wa Ido, anali woyang’anira Mahanaimu;
15 Ahimaazi anali woyang’anira Nafutali (iyeyu anakwatira Basemati mwana wa Solomoni);
16 Baana mwana wa Husai, anali woyang’anira Aseri ndi Bealoti;

[17] Yehosafati mwana wa Paruwa, anali woyang'anira Isakara;
[18] Simei mwana wa Ela, anali woyang'anira Benjamini;
[19] Geberi mwana wa Uri, anali woyang'anira Giliyadi (dziko la Sihoni mfumu ya Aamori ndi dziko la Ogi mfumu ya Basani). Iye ankayang'anira chigawo chonsechi yekha.

*Chakudya cha Tsiku ndi Tsiku cha Solomoni*

[20] Anthu a ku Yuda ndi ku Israeli anali ochuluka ngati mchenga wa
m'mbali mwa nyanja. Ankadya ndi kumwa ndipo ankasangalala. [21] Ndipo
Solomoni analamulira mayiko onse kuyambira ku mtsinje wa Yufurate mpaka ku dziko la Afilisti, kukafika mpaka ku malire a dziko la Igupto. Mayikowa ankabweretsa mphatso ndipo anali pansi pa ulamuliro wa Solomoni moyo wake wonse.

[22] Chakudya cha tsiku ndi tsiku cha Solomoni chinali madengu 150 a
ufa wosalala ndi madengu 300 a mgayiwa, [23] ng'ombe khumi zonenepa
zodyetsera m'khola, ng'ombe za ku busa makumi awiri, ndiponso nkhosa ndi mbuzi 100, pamodzinso ndi mbawala, agwape, mphoyo ndi mbalame
zoweta zonona. [24] Pakuti ankalamulira dziko lonse la kumadzulo kwa
mtsinje wa Yufurate kuyambira ku Tifisa mpaka ku Gaza, mafumu onse a kumadzulo kwa Mtsinje, ndipo anali pa mtendere ndi mayiko
onse ozungulira. [25] Pa nthawi ya Solomoni, Yuda ndi Israeli anali pa
mtendere, kuyambira ku Dani mpaka ku Beeriseba. Munthu aliyense ankangodzikhalira pansi pa mpesa wake ndi mtengo wake wa mkuyu.

[26] Solomoni anali ndi zipinda 4,000 zodyeramo akavalo okoka magaleta ake ndi anthu 12,000 oyendetsa magaleta.

[27] Abwanamkubwa a zigawo aja, aliyense pa mwezi wake, ankapereka chakudya cha Mfumu Solomoni ndi cha anthu onse amene ankadya
naye. Iwo ankaonetsetsa kuti pasasowe kalikonse. [28] Ankabweretsanso ku
malo ake ofunikira muyeso wawo wa barele ndi udzu wa akavalo okoka magaleta ndiponso akavalo ena.

*Nzeru za Solomoni*

[29] Mulungu anamupatsa Solomoni nzeru ndi luntha losaneneka ndipo nzeru zake zinali zochuluka ngati mchenga wa m'mbali mwa nyanja.
[30] Nzeru za Solomoni zinali zoposa nzeru za anthu onse a Kummawa
ndiponso nzeru zonse za ku Igupto. [31] Iye anali wanzeru kuposa munthu
wina aliyense, kuposa ngakhale Etani wa banja la Ezara, Hemani, Kalikoli ndi Darida, ana a Maholi. Ndipo mbiri yake inamveka kwa mitundu yonse
ya anthu ozungulira. [32] Solomoni anapeka miyambi 3,000 ndi kulemba
nyimbo 1,005. [33] Iye ankaphunzitsa za mitengo, kuyambira mtengo wa
mkungudza wa ku Lebanoni mpaka kachitsamba ka hisope khomera pa khoma. Iye ankaphunzitsanso za nyama ndi mbalame, zinthu zokwawa
pansi ndiponso za nsomba. [34] Anthu a mitundu yonse ankabwera
kudzamva nzeru za Solomoni. Anthu amenewa ankatumizidwa ndi mafumu onse a dziko lapansi amene anamvapo za nzeru zakezo.

# 5

*Kukonzekera Kumanga Nyumba ya Mulungu*

[1] Hiramu mfumu ya ku Turo atamva kuti Solomoni wadzozedwa kukhala mfumu m'malo mwa abambo ake Davide, anatumiza akazembe ake kwa

Solomoni, chifukwa mfumu Hiramu inali pa ubale wabwino ndi Davide
nthawi zonse. 2 Solomoni anabweza mawu awa kwa Hiramu:
3 "Inu mukudziwa kuti chifukwa cha nkhondo zimene zinkachokera
ku mbali zonse kulimbana ndi abambo anga, iwo sanathe kumangira
Nyumba Yehova Mulungu wawo, mpaka Yehova atawayika adani awo
pansi pa ulamuliro wawo. 4 Koma tsopano Yehova Mulungu wanga
wandipatsa mtendere mbali zonse za dziko ndipo ndilibe mdani kapena
chovuta chilichonse. 5 Choncho ine ndikufuna kumangira nyumba
Yehova Mulungu wanga, monga momwe Iye anawuzira abambo anga
Davide kuti, 'Mwana wako amene ndidzamukhazike pa mpando wau-
fumu m'malo mwako ndiye adzandimangire Nyumba.'
6 "Choncho lamulani kuti andidulire mikungudza ya ku Lebanoni. An-
thu anga adzagwira ntchito imeneyo pamodzi ndi anthu anuwo, ndipo
ine ndidzalipira anthu anuwo malipiro amene inu mungakhazikitse. Inu
mukudziwa kuti ife tilibe anthu aluso locheka matabwa monga Asidoni."
7 Hiramu anakondwa kwambiri atamva uthenga wa Solomoni ndipo
anati, "Lero Yehova atamandike chifukwa wapatsa Davide mwana
wanzeru kuti alamulire mtundu waukuluwu."
8 Tsono Hiramu anabweza mawu awa kwa Solomoni:
"Ndalandira uthenga umene mwanditumizira ndipo ine ndidzachita
zonse zimene mukufuna pokupatsani mitengo ya mkungudza ndi
payini. 9 Anthu anga adzatsika nayo kuchokera ku Lebanoni mpaka
ku nyanja, ndipo adzayiyandamitsa pa nyanja mpaka ku malo amene
munene. Kumeneko ndidzayimasula ndipo mudzayitenga. Ndipo inu
mudzakwaniritsa chokhumba changa pondipatsa chakudya cha banja
langa laufumu."
10 Motero Hiramu anapereka kwa Solomoni mitengo yonse ya mkun-
gudza ndi payini imene ankayifuna, 11 ndipo Solomoni anamupatsa
Hiramu mitanga ya tirigu 20,000 ngati chakudya cha pa nyumba yake,
kuwonjezera pa migolo ya mafuta a olivi yokwana 20,000. Solomoni
anapitiriza kupereka zimenezi chaka ndi chaka. 12 Yehova anamupatsa
Solomoni nzeru monga momwe analonjezera. Panali ubale wa mtendere
pakati pa Solomoni ndi Hiramu, ndipo awiriwa anachita pangano.
13 Mfumu Solomoni inasonkhanitsa anthu ogwira ntchito ya thangata
m'dziko lonse la Israeli ndipo anthu athangatawo analipo 30,000. 14 Iye
ankatumiza anthu 10,000 ku Lebanoni pa mwezi mosinthanasinthana,
kotero kuti ankakhala ku Lebanoniko mwezi umodzi ndipo kwawo
ankakhalako miyezi iwiri. Adoniramu ndiye ankayang'anira ogwira
ntchito yathangatayo. 15 Solomoni anali ndi anthu amtengatenga
70,000, anthu 80,000 osema miyala ku mapiri, 16 ndi akapitawo 33,000
amene ankayang'anira ntchitoyi ndiponso anthu ogwira ntchito zina.
17 Molamulidwa ndi mfumu, anakumba ndi kusema miyala ikuluikulu
kwambiri yoti akamangire maziko a Nyumba ya Mulungu. 18 Amisiri a
Solomoni ndi a Hiramu ndiponso anthu a ku Gebala anasema miyala ndi
kukonza matabwa ndi miyala yomangira Nyumba ya Mulungu.

# 6

*Solomoni Amanga Nyumba ya Mulungu*

1 Patapita zaka 480 Aisraeli atatuluka m'dziko la Igupto, chaka chachi-
nayi cha ulamuliro wa Solomoni mu Israeli, mwezi wa Zivi, umene ndi
mwezi wachiwiri, Solomoni anayamba kumanga Nyumba ya Yehova.

2 Nyumba imene Solomoni anamangira Yehova mulitali mwake inali
mamita 27, mulifupi mwake inali mamita asanu ndi anayi, ndipo msinkhu
wake unali mamita 13 ndi theka. 3 Chipinda chakubwalo m'mbali
mwake chinali mamita asanu ndi anayi kulingana ndi mulifupi mwa
Nyumbayo ndipo kutalika kwake kunali kwa mamita anayi ndi theka.
4 Anapanga mazenera amene maferemu ake anali olowa m'kati mwa
makoma a Nyumbayo. 5 M'mbali mwa makoma a Nyumba yayikulu
ndi chipinda chopatulika cham'kati, anamanga zipinda zosanjikizana,
mozungulira. 6 Chipinda chapansi, mulifupi mwake chinali mamita awiri,
chipinda chapakati mulifupi mwake chinali mamita awiri ndi theka ndipo
chipinda chapamwamba penipeni mulifupi mwake chinali mamita atatu.
Iye anapanga zinthu zosongoka kunja kwa khoma la kunja kuzungulira
Nyumbayo kuti asamapise kanthu pa makoma a Nyumba ya Mulungu.
7 Poyimanga Nyumbayo, anagwiritsa ntchito miyala yosemeratu, ndipo
pogwira ntchitoyo sipanamveke nyundo, nkhwangwa kapena chida china
chilichonse.
8 Chipata cholowera ku chipinda chapansi chinali mbali ya kummwera
kwa Nyumbayo. Panali makwerero okwerera ku chipinda chapakati
ndiponso chipinda cha pamwamba. 9 Choncho anamanga Nyumbayo
mpaka kuyimaliza ndipo denga lake linali la mitanda ndi matabwa a
mkungudza. 10 Msinkhu wa chipinda chilichonse unali mamita awiri,
ndipo anazilumukiza ku Nyumbayo ndi mitanda yamkungudza.
11 Yehova anayankhula ndi Solomoni kuti, 12 "Kunena za Nyumba
imene ukumangayi, ngati iwe udzamvera malangizo anga ndi kutsatira
mawu anga, ngati udzasunga malamulo anga ndi kuwachita, Ine ndidza-
kwaniritsa zonse zomwe ndinalonjeza Davide abambo ako. 13 Ndipo Ine
ndidzakhazikika pakati pa ana a Israeli ndipo sindidzawasiya anthu anga
Aisraeli."
14 Kotero Solomoni anamanga Nyumba ya Mulungu nayimaliza.
15 Anakuta khoma la m'kati mwake ndi matabwa a mkungudza, kuyam-
bira pansi pa Nyumbayo mpaka ku denga ndipo pansi pa Nyumbayo
anayalapo matabwa a payini. 16 Kumbuyo kwa Nyumbayo anadula
chipinda chachitali mamita asanu ndi anayi. Chipindachi anachimanga
ndi matabwa a mkungudza kuyambira pansi mpaka ku denga kuti
chikhale chipinda chopatulika cham'kati mwa Nyumba ya Mulungu ngati
Malo Wopatulika Kwambiri. 17 Chipinda chachikulu chimene chinali
kutsogolo kwa Malo Wopatulika Kwambiriwa, chinali mamita 18 mulitali
mwake. 18 M'kati mwa Nyumbayi munali matabwa a mkungudza, pamene
anajambulapo zithunzi za zikho ndi maluwa. Paliponse panali mkungudza
wokhawokha. Panalibe mwala uliwonse umene unkaonekera.
19 Anakonza malo wopatulika m'kati mwa Nyumbayi kuti ayikemo
Bokosi la Chipangano cha Yehova. 20 Malo wopatulika a m'katiwo anali
a mamita asanu ndi anayi mulitali mwake, mulifupi mwake, ndi msinkhu
wake. Anakuta m'kati mwake ndi golide weniweni ndiponso anapanga
guwa lansembe la matabwa a mkungudza. 21 Solomoni anakutira golide
weniweni m'kati mwake mwa Nyumbayi, ndipo anayalika maunyolo a
golide mopingasa kutsogolo kwa malo wopatulika amene anakutidwa ndi
golide. 22 Motero anakuta m'kati monse ndi golide. Anakutanso ndi golide
guwa lansembe la m'kati mwa chipinda chopatulika.
23 M'chipinda chopatulika cha m'kati anapangamo akerubi awiri a
mtengo wa olivi. Msinkhu wa kerubi aliyense unali mamita anayi ndi
theka. 24 Phiko limodzi la kerubi kutalika kwake kunali mamita awiri ndi

theka, phiko linanso linali mamita awiri ndi theka, kutambasula mapiko
awiriwo, kuchokera msonga ina mpaka msonga ina kutalika kwake
kunali mamita anayi ndi theka. 25 Kerubi wachiwiriyo msinkhu wake
unalinso mamita anayi ndi theka, pakuti akerubi awiriwo anali a misinkhu
yofanana ndi a mapangidwe ofanana. 26 Msinkhu wa kerubi aliyense unali
mamita anayi ndi theka. 27 Solomoni anayika akerubiwo m'chipinda cha
m'kati mwenimweni mwa Nyumba ya Mulungu, atatambasula mapiko
awo. Phiko la kerubi wina limakhudza khoma lina, pamene phiko la
winayo limakhudza khoma linanso ndipo mapiko awo amakhudzana
pakati pa chipindacho. 28 Akerubiwo anawakuta ndi golide.

29 Pa makoma onse kuzungulira Nyumbayo, m'zipinda za m'kati ndi
za kunja zomwe, anajambulapo akerubi, mitengo ya mgwalangwa ndi
maluwa. 30 Anayala golide pansi mu Nyumbamo m'zipinda zam'kati ndi
zakunja zomwe.

31 Ndipo pa khomo lolowera ku malo wopatulika am'kati anapanga
zitseko za mtengo wa olivi ndipo khonde lake linali ndi mbali zisanu.
32 Ndipo pa zitseko ziwiri zija za mtengo wa olivi anajambulapo kerubi,
mitengo ya mgwalangwa ndi maluwa ndipo anapaka golide akerubiwo ndi
mitengo ya mgwalangwayo. 33 Anapanganso chimodzimodzi mphuthu za
mbali zinayi za mtengo wa olivi za pa khomo la Nyumbayo. 34 Solomoni
anapanganso zitseko ziwiri za payini. Chitseko chilichonse chinali ndi
mbali ziwiri zotha kuzipinda. 35 Pa zitsekozo anagobapo akerubi, mitengo
ya mgwalangwa ndi maluwa wotambasuka ndipo zojambulazo anazikuta
ndi golide wopyapyala.

36 Ndipo anamanga bwalo la m'kati lokhala ndi khoma lokhala ndi
mizere itatu ya miyala yosema ndiponso mzere umodzi wa matabwa
osemedwa a mkungudza.

37 Maziko a Nyumba ya Yehova anamangidwa pa chaka chachinayi,
mwezi wa Zivi. 38 Pa chaka cha 11 mwezi wa Buli, mwezi wachisanu
ndi chitatu, madera onse a Nyumba anatha kumangidwa monga momwe
kunkafunikira. Anamanga Nyumbayo kwa zaka zisanu ndi ziwiri.

# 7

*Solomoni Amanga Nyumba Yake Yaufumu*

1 Solomoni anamanga nyumba yake yaufumu kwa zaka 13. 2 Iye
anamanga nyumba yaufumu yotchedwa Nkhalango ya Lebanoni yomwe
mulitali mwake inali mamita 44, mulifupi mwake mamita 22, msinkhu
wake mamita 13 ndi theka; ndipo inakhazikika pa mizere inayi ya ma-
panda a mkungudza yokhala ndi mitanda ya mkungudza yotanthalika pa
mapandawo. 3 Pamwamba pa mitandapo panali matabwa a mkungudza
amene anaphimba zipinda zimene zinamangidwa pa nsanamira 45, pa
mzere uliwonse nsanamira 15. 4 Mazenera a nyumbayo anali mmwamba
m'mizere itatu, zenera kuyang'anana ndi zenera linzake. 5 Zitseko zonse
ndi mazenera omwe, maferemu ake anali ofanana mbali zonse. Mulitali
mwake ndi mulifupi mwake, ndipo zenera linkapenyana ndi zenera
linzake pa mizere itatu.

6 Iye anapanga Chipinda cha Nsanamira. Mulitali mwake munali
mamita 22, mulifupi mwake munali mamita 13 ndi theka. Patsogolo pake
panali khonde ndi nsanamira zokhala ndi denga.

7 Anamanga chipinda cha mpando waufumu, Chipinda cha Chilungamo,
modzaweruziramo milandu ndipo anayikutira ndi matabwa a mkungudza

kuchokera pansi mpaka ku denga. 8 Ndipo nyumba yake yodzakhalamo
anayimanga kumbuyo kwa chipindacho. Nyumbayo anayimanga mo-
fanana ndi Chipindacho. Solomoni anamanga nyumba inanso yofanana
ndi chipindachi, kumangira mkazi wake mwana wa Farao.

9 Nyumba zonsezi, kuyambira kunja mpaka ku bwalo lalikulu ndiponso
kuchokera pa maziko mpaka pamwamba pa khoma, zinapangidwa ndi
miyala yabwino kwambiri imene anayisema potengera miyeso yake
yoyenera ndipo anayisalaza ndi macheka m'kati ndi kunja komwe.
10 Maziko ake anali a miyala yabwino kwambiri, kutalika kwa miyala
ina kunali mamita atatu ndi theka, inanso mamita anayi. 11 Pamwamba
pake panali pa miyala yabwino kwambiri, yosemedwa potengera miyeso
yake. Pamwamba pa miyalayo panali matabwa a mkungudza. 12 Bwalo
lalikulu lozungulira nyumbayi linali ndi khoma la mizere itatu ya miyala
yosemedwa ndi mzere umodzi wa matabwa a mkungudza. Bwalo la m'kati
la Nyumba ya Yehova ndiponso khonde lake anazimanga mofanana.

### *Zipangizo za m'Nyumba ya Mulungu*

13 Mfumu Solomoni anatuma anthu ku Turo ndipo anakabwera ndi
Hiramu, 14 mwana wa mkazi wamasiye wa fuko la Nafutali ndipo abambo
ake anali a ku Turo, m'misiri wa mkuwa. Hiramu anali munthu wa luso
lalikulu ndiponso wodziwa kupanga zinthu za mkuwa. Iye anabwera kwa
Mfumu Solomoni ndi kugwira ntchito zonse zimene anamupatsa.

15 Iye anawumba nsanamira ziwiri za mkuwa, nsanamira iliyonse
msinkhu wake unali mamita asanu ndi atatu ndipo thunthu lake akazun-
guliza chingwe, linali mamita asanu ndi theka. 16 Anapanganso mitu iwiri
ya mkuwa ndi kuyiika pamwamba pa nsanamira zija; mutu uliwonse
unali wotalika kupitirirapo mamita awiri. 17 Pa mitu ya pa nsanamirazo
anakolekapo maunyolo awiri olukanalukana ndi oyangayanga. Mutu
uliwonse unali ndi maunyolo oterewa asanu ndi awiri. 18 Anapanga
mizere iwiri ya zinthu zonga makangadza mozungulira pamwamba pa
maunyolo kukongoletsa mitu ya nsanamirazo. Anachita chimodzimodzi
ndi mutu uliwonse. 19 Mitu imene inali pamwamba pa nsanamira
m'khonde inali yooneka ngati maluwa okongola kwambiri. Kutalika
kwake kunali pafupifupi mamita awiri. 20 Pa mitu yonse iwiri ya
pamwamba pa nsanamira, pamwamba pa chigawo chonga m'phika pafupi
ndi cholukidwa ngati ukonde, panali makangadza 200 okhala mozungulira
m'mizere. 21 Anayimika nsanamirazo pa khonde la Nyumba ya Mulungu.
Nsanamira ya kumpoto anayitcha Yakini ndipo ya kummwera anayitcha
Bowazi. 22 Mitu ya pamwamba pa nsanamirazo inali yooneka ngati
maluwa okongola kwambiri. Motero anamaliza ntchito ya nsanamirazo.

23 Kenaka iye anapanga mbiya yayikulu yachitsulo. Inali yozungulira
ndipo pakamwa pake panali pa mamita anayi ndi theka, poyeza modutsa
pakati pake. Msinkhu wake unali wopitirirapo mamita awiri. Thunthu
lake linali mamita 13. 24 M'munsi mwa mkombero wa mbiyayo anajam-
bulamo tizikho kuzungulira thunthu lonse la mbiyayo, tizikho khumi pa
theka la mita. Tizikhoto tinali m'mizere iwiri ndipo anatipangira kumodzi
ndi mbiyayo.

25 Mbiyayo anayisanjika pa ng'ombe zamkuwa khumi ndi ziwiri, zitatu
zoyang'ana kumpoto, zitatu zoyang'ana kumadzulo, zitatu zoyang'ana
kummwera ndipo zitatu zoyang'ana kummawa. Mbiyayo inakhazikika
pamwamba pa ng'ombezo, ndipo miyendo yake yonse yakumbuyo ya
ng'ombezo inkaloza m'kati. 26 Mbiyayo inali yonenepa ngati chikhatho

ndipo mkombero wake unali ngati mkombero wa chikho, ngati duwa lokongola kwambiri. M'mbiyamo munkalowa madzi okwana malita 40,000.

27 Iye anapanganso maphaka khumi a mkuwa. Phaka lililonse mulitali
mwake linali pafupifupi mamita awiri, mulifupi mwake linali pafupifupi
mamita awiri, ndipo msinkhu wake unali kupitirirapo mita imodzi.
28 Maphakawo anapangidwa motere: Anali ndi matabwa a m'mbali
amene ankalowa m'maferemu. 29 Pakati pa matabwa a m'mbali ndi
maferemu panali zithunzi za mikango, ng'ombe zazimuna ndi akerubi. Pa maferemuwo, pamwamba ndi pansi pake pa mikangoyo ndi ng'ombe
zazimunazo anajambulapo nkhata za maluwa. 30 Phaka lililonse linali
ndi mikombero ya mkuwa inayi ndi mitandanso ya mkuwa, ndipo phaka lililonse linali ndi zogwiriziza mbale zosambira pa ngodya zake zinayi,
zopangidwa limodzi ndi nkhata za maluwa mbali zake zonse. 31 M'kati
mwa phakalo munali malo otsekuka amene anali ndi feremu yozungulira ndipo anali ozama theka la mita. Malo otsekukawa anali wozungulira, ndipo pamodzi ndi tsinde lake anali otalika masentimita 44. Kuzungulira pa malo otsekukawa panajambulidwa zokometsera. Matabwa oyimikira phakali anali ofanana mbali zonse, osati ozungulira. 32 Pansi pa
matabwawo panali mikombero inayi, ndipo mitanda ya mikomberoyo inalumikizidwa ku phakalo. Msinkhu wa mkombero uliwonse unali
masentimita 66. 33 Mikomberoyo inapangidwa ngati mikombero ya galeta;
mitanda yake, marimu ake, sipokosi zake ndiponso mahabu ake, zonsezi zinali za chitsulo.

34 Phaka lililonse linali ndi zogwirira zinayi; chogwirira chimodzi pa
ngodya iliyonse, zolumikizidwa ku phakalo. 35 Pamwamba pa phakalo
panali mkombero wozungulira ndipo msinkhu wake unali masentimita 22. Pamwamba pa phakalo panali zogwiriziza ndi matabwa ake,
zolumikizidwa ku phakalo. 36 Paliponse pamene panali malo woti
n'kujambulapo, pa zogwiriziza ndi pa matabwa, anagobapo zithunzi za akerubi, mikango ndi mitengo ya mgwalangwa. Anajambulanso nkhata za
maluwa mozungulira. 37 Umu ndi mmene anapangira maphaka khumiwo.
Onse anawapanga malo ofanana ndipo anali a miyeso yofanana ndiponso wooneka mofanana.

38 Kenaka anapanga mabeseni akuluakulu khumi a mkuwa; beseni
lililonse munkalowa madzi a malita 800, ndipo poyeza modutsa, pakamwa pake panali pafupifupi mamita awiri. Maphaka khumi aja, lililonse linali
ndi beseni lake. 39 Maphaka asanu anawayika mbali ya kummwera
kwa Nyumba ya Mulungu, asanu enawo anawayika mbali ya kumpoto. Mbiyayo anayiyika mbali yakummwera, pa ngodya yakummwera cha
kummawa kwa Nyumba ya Mulungu. 40 Iye anapanganso miphika ndi
mafosholo ndi mabeseni owazira magazi.

Kotero Hiramu anatsiriza ntchito yonse ya ku Nyumba ya Yehova imene ankagwirira Mfumu Solomoni:

41 nsanamira ziwiri;
mbale ziwiri za mitu yapamwamba pa nsanamirazo;
maukonde awiri okongoletsera mbale ziwiri za mitu yapamwamba pa nsanamirazo;
42 makangadza 400 a maukonde awiri okongoletserawo (mizere iwiri ya makangadza pa ukonde uliwonse, kukongoletsa mbale za mitu yapamwamba pa nsanamira);

43 maphaka khumi pamodzi ndi mabeseni khumi pa maphakawo;
44 mbiya pamodzi ndi ng'ombe khumi ndi ziwiri zazimuna zosanjikapo mbiyayo;
45 miphika, mafosholo ndi mbale zowazira magazi.

Ziwiya zonsezi za ku Nyumba ya Yehova, zimene Hiramu anapangira
Mfumu Solomoni, zinali zamkuwa wonyezimira. 46 Mfumu inapangitsa
zimenezi m'chigwa cha Yorodani, ku malo amtapo amene anali pakati pa
Sukoti ndi Zaretani. 47 Solomoni sanayeze ziwiya zonsezi chifukwa zinali
zambiri ndipo kulemera kwa mkuwa sikunadziwike.
48 Solomoni anapanganso ziwiya zonse zimene zinali m'Nyumba ya
Yehova:

guwa lansembe lagolide;
tebulo lagolide pamene ankayikapo buledi woperekedwa kwa Mulungu;
49 zoyikapo nyale zagolide weniweni (dzanja lamanja zisanu ndipo zisanu zina ku dzanja lamanzere, m'kati mwenimweni mwa malo opatulika);
maluwa agolide, nyale ndi mbaniro;
50 mbale zagolide weniweni, zozimitsira nyale, mbale zowazira magazi, mbale ndi zofukizira;
ndiponso zomangira zitseko zagolide za chipinda cham'kati mwenimweni, Malo Opatulika Kwambiri, ndiponso za zitseko za chipinda chachikulu cha Nyumba ya Mulungu.

51 Pamene ntchito yonse imene Mfumu Solomoni inagwira pa Nyumba
ya Yehova inatha, anabwera ndi zinthu zonse zimene abambo ake Davide
anazipereka: siliva, golide ndi ziwiya. Anaziyika m'zipinda zosungiramo
chuma cha ku Nyumba ya Yehova.

# 8

### *Abwera ndi Bokosi la Chipangano ku Nyumba ya Yehova*

1 Pamenepo Mfumu Solomoni inasonkhanitsa akuluakulu a Israeli,
atsogoleri onse a mafuko ndi akuluakulu a mabanja a Aisraeli mu
Yerusalemu, kuti akatenge Bokosi la Chipangano la Yehova ku Ziyoni,
Mzinda wa Davide. 2 Aisraeli onse anasonkhana pamaso pa Mfumu
Solomoni nthawi ya chikondwerero cha mwezi wa Etanimu, mwezi
wachisanu ndi chiwiri.
3 Akuluakulu onse a Israeli atafika, ansembe ananyamula Bokosi la
Chipangano, 4 ndipo anabwera nalo Bokosi la Yehova pamodzi ndi tenti
ya msonkhano ndi ziwiya zonse zopatulika zimene zinali m'menemo.
Ansembe ndi Alevi ndiye anazinyamula, 5 ndipo Mfumu Solomoni ndi
gulu lonse la Aisraeli amene anasonkhana naye anali patsogolo pa Bokosi
la Chipangano, akupereka nsembe nkhosa zambiri ndi ng'ombe zambiri
zosawerengeka.
6 Ansembe anafika nalo Bokosi la Chipangano la Yehova m'chipinda
cham'kati mwenimweni, Malo Opatulika Kwambiri, ndipo analiyika pansi
pa mapiko a akerubi. 7 Akerubiwo anatambalitsa mapiko awo pamwamba
pa Bokosi la Chipangano ndipo anaphimba bokosilo pamodzi ndi mitengo
yonyamulira. 8 Mitengoyi inali yayitali kwambiri ndipo inkaonekera
kunja kwa chipinda cham'kati cha Malo Opatulika koma osati kunja kwa

Malo Opatulikawo; ndipo mitengoyi ilipo mpaka lero lino. 9 M'bokosimo
munalibe kanthu kena kalikonse kupatula miyala iwiri imene Mose
anayikamo ku Horebu, kumene Yehova anachita pangano ndi Aisraeli
atatuluka m'dziko la Igupto.

10 Ansembe atatuluka m'Malo Opatulikawo, mtambo unadzaza Nyumba
ya Yehova. 11 Ndipo ansembewo sanathe kugwira ntchito yawo chifukwa
cha mtambowo, pakuti ulemerero wa Yehova unadzaza m'Nyumba ya
Yehova.

12 Pamenepo Solomoni anati, "Yehova anati adzakhala m'mitambo
yakuda; 13 taonani ndithu, ine ndakumangirani Nyumba yokongola
kwambiri, malo woti muzikhalamo mpaka muyaya."

14 Aisraeli onse ali chiyimire pomwepo, mfumu inatembenuka ndi
kuwadalitsa. 15 Ndipo inati:

"Atamandike Yehova, Mulungu wa Israeli, amene wachita ndi dzanja
lake zimene analonjeza ndi pakamwa pake kwa Davide abambo anga.
Pakuti Iye anati, 16 'Kuyambira tsiku limene ndinatulutsa anthu anga
Aisraeli ku Igupto, sindinasankhe mzinda wina uliwonse pa fuko
lina lililonse la Aisraeli kuti kumeneko andimangire Nyumba, koma
ndasankha Davide kuti alamulire anthu anga Aisraeli.'

17 "Abambo anga Davide anali ndi maganizo mu mtima mwawo
oti amangire nyumba Yehova, Mulungu wa Israeli. 18 Koma Yehova
ananena kwa abambo anga, Davide, kuti, 'Popeza zinali mu mtima
mwako kumangira nyumba Dzina langa, unachita bwino kukhala ndi
maganizo amenewa mu mtima mwakomo. 19 Komatu, si iwe amene
udzamanga Nyumba ya Mulungu, koma mwana wako, mwana amene
iwe udzabereke. Iyeyo ndiye adzandimangire Nyumba.'

20 "Yehova wasunga zimene analonjeza: ine ndalowa m'malo mwa
abambo anga Davide ndipo tsopano ndili pa mpando waufumu wa
Israeli, monga momwe Yehova analonjezera, ndipo ndamangira nyumba
Dzina la Yehova, Mulungu wa Israeli. 21 Ndalikonzera malo Bokosi la
Chipangano mmene muli pangano la Yehova limene anapangana ndi
makolo athu pamene anawatulutsa m'dziko la Igupto."

### *Pemphero Lodzipereka la Solomoni*

22 Pamenepo Solomoni anayimirira patsogolo pa guwa lansembe la
Yehova pamaso pa gulu lonse la Aisraeli ndipo anakweza manja ake
kumwamba, 23 nati:

"Inu Yehova, Mulungu wa Israeli, palibe Mulungu wofanana nanu
kumwamba kapena pansi pa dziko, inu amene mumasunga pangano
ndi kuonetsa chikondi chosasinthika kwa atumiki anu amene amayenda
pamaso panu ndi mtima wawo wonse. 24 Inu mwasunga lonjezo lanu
kwa abambo anga Davide, mtumiki wanu. Inde zimene munalonjeza
ndi pakamwa panu, mwazikwaniritsa ndi manja anu, monga mmene
tikuonera lero lino.

25 "Ndipo tsopano, Inu Yehova Mulungu wa Israeli, sungani zimene
munalonjeza kwa abambo anga Davide, mtumiki wanu, pamene munati,
'Sudzasowa munthu wokhala pamaso panga pa mpando waufumu wa
Israeli, ngati ana ako adzasamalira mayendedwe awo mokhulupirika
monga iwe wachitira.' 26 Ndipo tsopano, Inu Mulungu wa Israeli, lolani
kuti mawu anu akwaniritsidwe amene munalonjeza mtumiki wanu
Davide abambo anga.

27 “Kodi Mulungu angakhaledi pa dziko lapansi? Mlengalenga
ngakhale kumwamba kwenikweni, sikungakukwaneni. Nanga kuli
bwanji ndi Nyumba iyi imene ndamanga! 28 Koma Inu Yehova Mulungu
wanga, imvani pemphero ndi pembedzero la mtumiki wanu. Imvani
kulira ndi pemphero la mtumiki wanu limene ndikupempha pamaso
panu lero lino. 29 Maso anu azikhala otsekuka kuyang’ana Nyumba ino
usiku ndi usana, malo ano amene Inu munanena kuti, ‘Dzina langa
lidzakhala m’menemo,’ choncho imvani pemphero limene mtumiki
wanu akupemphera akuyang’ana malo ano. 30 Imvani pembedzero
la mtumiki wanu ndi la anthu anu Aisraeli pamene akupemphera
akuyang’ana malo ano. Imvani kumwambako, malo anu amene
mumakhala; ndipo mukamva muzitikhululukira.

31 “Munthu akalakwira mnzake, nawuzidwa kuti alumbire, akabwera
kudzalumbira patsogolo pa guwa lansembe la Nyumba ino, 32 imvani
kumwambako ndi kuchitapo kanthu. Weruzani atumiki anuwo,
wochimwa mugamule kuti ndi wolakwa ndipo alangidwe chifukwa cha
zimene wachita. Wosachimwa mugamule kuti ndi wosalakwa, ndipo
muonetse kusalakwa kwakeko.

33 “Anthu anu Aisraeli akagonja kwa adani awo chifukwa
akuchimwirani, ndipo akatembenukira kwa Inu ndi kuvomereza
Dzina lanu, kupemphera ndi kupembedzera kwa Inu m’Nyumba ino,
34 pamenepo imvani kumwambako ndi kukhululukira tchimo la anthu
anu Aisraeli ndi kuwabweretsa ku dziko limene munawapatsa makolo
awo.

35 “Pamene kumwamba kwatsekeka ndipo mvula sikugwa chifukwa
anthu anu akuchimwirani, ndipo pamene apemphera akuyang’ana
malo ano ndi kuvomereza Dzina lanu, ndi kutembenuka kuchoka
ku machimo awo chifukwa inu mwawalanga, 36 pamenepo imvani
kumwambako ndipo muwakhululukire atumiki anu, anthu anu Aisraeli.
Aphunzitseni makhalidwe oyenera ndipo gwetsani mvula m’dziko
limene munapereka kwa anthu anu monga cholowa chawo.

37 “Pamene m’dziko mwagwa njala kapena mliri, chinoni kapena
chiwawu, dzombe kapena kapuchi, kapena pamene mdani wazungulira
mzinda wawo wina uliwonse, kaya mavuto kapena matenda abwera,
38 ndipo wina aliyense mwa Aisraeli akapemphera kapena kukudan-
daulirani, aliyense wa iwo akadziwa masautso a mu mtima mwake
ndi kukweza manja awo kuloza Nyumba ino, 39 pamenepo imvani
kumwambako, malo anu wokhalamo. Khululukani ndipo chitanipo
kanthu. Muchitire aliyense molingana ndi zonse zimene anachita,
popeza inu mumadziwa mtima wake (pakuti ndinu nokha amene
mumadziwa mitima ya anthu onse), 40 motero iwo adzakuopani masiku
onse amene adzakhale m’dziko limene munalipereka kwa makolo athu.

41 “Ndipo kunena za mlendo amene si mmodzi wa anthu anu Aisraeli,
koma wabwera kuchokera ku dziko lakutali chifukwa cha dzina lanu,
42 pakuti anthu adzamva za dzina lanu lotchukali ndiponso za dzanja
lanu lamphamvu ndi lochita zazikulu, kudzapemphera akuyang’ana
Nyumba ino, 43 pamenepo imvani kumwambako, malo anu okhalamo,
ndipo muchite zonse zimene mlendoyo akukupemphani, kotero kuti
anthu onse a dziko lapansi adziwe dzina lanu ndi kukuopani monga
amachitira anthu anu Aisraeli, ndipo adziwe kuti Nyumba ino imene
ndakumangirani imadziwika ndi Dzina lanu.

44 “Pamene anthu anu apita ku nkhondo kukamenyana ndi adani
awo, kulikonse kumene mungawatume, ndipo pamene apemphera kwa

Yehova moyang'ana mzinda umene mwausankha ndi Nyumba imene
ine ndamangira Dzina lanu, 45 imvani kumwambako pemphero lawo
ndi kudandaula kwawo, ndipo apambanitseni.

46 "Pamene akuchimwirani, popeza palibe munthu amene sachimwa,
ndipo Inu n'kuwakwiyira ndi kuwapereka kwa mdani, amene adza-
watenga ukapolo kupita ku dziko lake, kutali kapena pafupi; 47 ndipo
ngati asintha maganizo ali ku dziko la ukapololo ndi kulapa ndi kuku-
dandaulirani m'dziko la owagonjetsa ndi kunena kuti, 'Ife tachimwa,
tachita zolakwa, tachita zinthu zoyipa,' 48 ndipo ngati abwerera kwa
Inu ndi mtima wawo wonse ndi moyo wawo wonse m'dziko la adani
awo amene anawatenga ukapolo, ndi kupemphera kwa Inu moyang'ana
dziko limene munapereka kwa makolo awo, moyang'ana mzinda umene
munawusankha ndiponso Nyumba imene ine ndamangira Dzina lanu,
49 imvani kumwambako, malo anu wokhalamo, imvani pemphero lawo
ndi kudandaula kwawo, ndipo muwachitire zabwino. 50 Ndipo khulu-
lukirani anthu anu amene akuchimwirani. Khululukirani zolakwa zonse
akuchitirani ndipo mufewetse mitima ya amene anawagonjetsawo kuti
awachitire chifundo; 51 popeza ndi anthu anu ndiponso cholowa chanu,
anthu omwe munawatulutsa ku Igupto, kuwachotsa m'ng'anjo yamoto
yosungunula zitsulo.

52 "Maso anu atsekuke kuti aone dandawulo la mtumiki wanu
ndiponso madandawulo a anthu anu Aisraeli, ndipo mutchere khutu
nthawi iliyonse pamene akulirirani. 53 Pakuti Inu munawasiyanitsa ndi
anthu a mitundu ina yonse ya dziko lonse kuti akhale cholowa chanu,
monga momwe munanenera kudzera mwa mtumiki wanu Mose pamene
Inu, Ambuye Yehova, munatulutsa makolo athu ku Igupto."

54 Solomoni atamaliza mapemphero ndi mapembedzero onsewa kwa
Yehova, anayimirira pa guwa lansembe la Yehova, nagwada atakweza
manja ake kumwamba. 55 Anayimirira ndi kudalitsa gulu lonse la Aisraeli
ndi mawu okweza, nati:

56 "Atamandike Yehova, amene wapereka mpumulo kwa anthu ake
Aisraeli monga momwe analonjezera. Palibe mawu ndi amodzi
omwe amene anapita pachabe pa malonjezo ake onse abwino amene
anawapereka kudzera mwa mtumiki wake Mose. 57 Yehova Mulungu
wathu akhale nafe monga momwe anakhalira ndi makolo athu; asatisiye
kapena kutitaya. 58 Atembenuzire mitima yathu kwa Iye, kuti tiyende
m'njira zake zonse ndi kusunga mawu ake, malamulo ake ndi malangizo
ake amene anapereka kwa makolo athu. 59 Ndipo mawu angawa,
amene ndapemphera pamaso pa Yehova, asayiwalike pamaso pa Yehova
Mulungu wathu usana ndi usiku, ndipo Iye alimbikitse mtumiki wake
ndiponso athandize Aisraeli, anthu ake powapatsa zosowa zawo za
tsiku ndi tsiku, 60 kotero kuti anthu a mitundu yonse pa dziko lapansi
adziwe kuti Yehova ndi Mulungu ndipo kuti palibenso wina. 61 Koma
mitima yanu ikhale yodzipereka kwathunthu kwa Yehova Mulungu
wanu, kutsatira malamulo ake ndi kumvera malangizo ake, monga lero
lino."

### *Mwambo Wopereka Nyumba ya Mulungu*

62 Ndipo mfumu pamodzi ndi Aisraeli onse anapereka nsembe pamaso
pa Yehova. 63 Solomoni anapereka nsembe zachiyanjano kwa Yehova:
ng'ombe 22,000, nkhosa ndi mbuzi 120,000. Motero mfumu pamodzi ndi
Aisraeli onse anapatula Nyumba ya Yehova.

64 Tsiku lomwelo mfumu inapatulanso malo a pakati pa bwalo limene
linali kutsogolo kwa Nyumba ya Yehova ndiponso nthuli za mafuta za
nsembe yachiyanjano, chifukwa guwa lansembe la mkuwa limene linali
pamaso pa Yehova linali lochepa kwambiri ndipo nsembe zonse zopsereza,
nsembe zachakudya, ndi nthuli za mafuta a nsembe zachiyanjano
sizikanakwanirapo.
65 Choncho nthawi imeneyi, Solomoni anachita chikondwerero pamodzi
ndi Aisraeli onse. Unali msonkhano waukulu, kuyambira ku Lebo
Hamati mpaka ku Chigwa cha ku Igupto. Anachita chikondwerero
chimenechi pamaso pa Yehova Mulungu wathu kwa masiku asanu ndi
awiri, anawonjezerapo masiku ena asanu ndi awiri, onse pamodzi ngati
masiku 14. 66 Pa tsiku lachisanu ndi chitatu Solomoni anawuza anthu
kuti apite kwawo. Anthuwo anathokoza mfumu ndipo kenaka anapita
kwawo mokondwa ndi mosangalala m'mitima mwawo chifukwa cha
zinthu zabwino zimene Yehova anachitira mtumiki wake Davide ndi anthu
ake Aisraeli.

# 9

*Yehova Aonekera Solomoni*

1 Solomoni atatsiriza kumanga Nyumba ya Yehova ndi nyumba yau-
fumu, ndi kukwaniritsa kuchita zonse zimene ankafuna, 2 Yehova
anamuonekera kachiwiri, monga momwe anamuonekera ku Gibiyoni.
3 Yehova ananena kwa iye kuti:

"Ndamva pemphero ndi pembedzero lako pa zimene wapempha
pamaso panga. Ndayipatula Nyumba iyi, imene wamanga, poyikamo
Dzina langa mpaka muyaya. Maso anga ndi mtima wanga zidzakhala
pamenepo nthawi zonse.

4 "Kunena za iwe, ukayenda pamaso panga mokhulupirika, mwang-
wiro ndi moona mtima monga momwe anachitira abambo ako Davide,
ndi kuchita zonse zimene ndakulamula ndi kusamalitsa malangizo
ndi malamulo anga, 5 Ine ndidzakhazikitsa mpando wako waufumu
pa Israeli mpaka muyaya, monga ndinalonjezera abambo ako Davide
pamene ndinati, 'Sipadzasowa munthu pa mpando waufumu wa Israeli.'

6 "Koma ngati iwe kapena ana ako mudzapatuka ndi kuleka kusunga
malamulo ndi mawu anga amene ndakupatsani ndi kupita kukatumikira
milungu ina ndi kuyipembedza, 7 pamenepo Ine ndidzazula Aisraeli
m'dziko limene ndinawapatsa ndiponso ndidzayikana Nyumba ino
imene ndayipatula chifukwa cha Dzina langa. Pamenepo Aisraeli
adzasanduka mwambi ndi chinthu chonyozedwa pakati pa anthu onse.
8 Ndipo ngakhale kuti tsopano Nyumba ya Mulunguyi ndi yokongola
kwambiri, onse amene adzadutsa pano adzadabwa kwambiri ndipo
adzatsonya ndipo adzati, 'N'chifukwa chiyani Yehova wachita chinthu
chotere m'dziko muno ndi pa Nyumba ya Mulunguyi?' 9 Anthu
adzayankha kuti, 'N'chifukwa chakuti asiya Yehova Mulungu wawo
amene anatulutsa makolo awo m'dziko la Igupto, ndipo akangamira
milungu ina ndi kumayipembedza ndi kuyitumikira. Choncho Iye
wabweretsa zovuta zonsezi.' "

*Zina zimene Solomoni Anachita*

10 Patatha zaka makumi awiri, ndiye nthawi imene Solomoni anamanga
nyumba ziwirizi: Nyumba ya Yehova ndi nyumba yaufumu, 11 Mfumu
Solomoni anapereka mizinda makumi awiri ya ku Galileya kwa Hiramu

mfumu ya ku Turo chifukwa Hiramu n'kuti atapereka mitengo yonse ya mkungudza ndi ya payini ndiponso golide yense zimene Solomoni ankaz-
ifuna. [12] Koma Hiramu atabwera kuchokera ku Turo kudzaona mizinda imene Solomoni anamupatsa, sanasangalatsidwe nayo mizindayo. [13] Iye
anafunsa kuti, "M'bale wanga, kodi iyi n'kukhala mizinda yondipatsa?" Ndipo iye anayitcha mizindayo Dziko la Kabuli, dzina lomwe amatchedwa mpaka lero lino. [14] Koma Hiramu anali atatumiza kwa mfumu golide
oposa makilogalamu 4,000.

[15] Izi ndi zimene anachita Mfumu Solomoni: Analamula anthu kuti agwire ntchito yathangata pomanga Nyumba ya Yehova, nyumba yake, malo achitetezo a Milo, mpanda wa Yerusalemu, Hazori, Megido ndi
Gezeri. [16] (Farao mfumu ya ku Igupto inali itathira nkhondo ndi kulanda Gezeri. Iye anatentha mzindawo. Anapha Akanaani amene ankakhala m'menemo ndipo kenaka anawupereka ngati mphatso yaukwati kwa mwana wake wamkazi amene anakwatiwa ndi Solomoni. [17] Ndipo
Solomoni anamanganso Gezeri.) Iye anamanga Beti-Horoni Wakumunsi,
[18] Baalati ndi Tadimori ku chipululu, m'dziko lake lomwelo, [19] pamodzinso
ndi mizinda yake yosungira chuma ndiponso mizinda yosungiramo magaleta ndi akavalo ake. Anamanganso chilichonse chimene anafuna kumanga ku Yerusalemu, ku Lebanoni ndi ku madera onse amene iye ankalamulira.

[20] Panali anthu amene anatsala pakati pa mitundu ya Aamori, Ahiti,
Aperezi, Ahivi ndi Ayebusi (anthu awa sanali Aisraeli). [21] Zimenezi ndiye
zinali zidzukulu zawo zotsalira m'dzikoli, anthu amene Aisraeli sanathe kuwawononga kotheratu. Solomoni anawatenga ndi kukhala akapolo ake ogwira ntchito yathangata, monga zilili mpaka lero lino. [22] Koma
Solomoni sanagwiritse ntchito ya ukapolo Mwisraeli aliyense; iwo anali anthu ake ankhondo, nduna zake, atsogoleri a ankhondo, akapitawo ake,
olamulira magaleta ndi oyendetsa magaleta ake. [23] Amenewa ndiwo anali
akuluakulu oyang'anira ntchito za Solomoni. Anthu okwana 550 ndiwo ankayang'anira anthu amene ankagwira ntchitowo.

[24] Mwana wamkazi wa Farao atachoka mu Mzinda wa Davide, kupita ku nyumba ya mfumu imene Solomoni anamumangira, Solomoni anamanga malo achitetezo a Milo.

[25] Katatu pa chaka Solomoni ankapereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano pa guwa lansembe limene anamangira Yehova ndiponso ankafukiza lubani pamaso pa Yehova. Potero ankakwaniritsa zoyenera kuchitika mu Nyumba ya Yehova.

[26] Mfumu Solomoni anapanganso sitima zapamadzi ku Ezioni Geberi, malo amene ali pafupi ndi Eloti ku Edomu, m'mbali mwa Nyanja Yofiira.
[27] Ndipo Hiramu anatumiza anthu ake oyendetsa sitima zapamadzi amene
ankadziwa za pa nyanja kuti aziyendetsa pamodzi ndi anthu a Solomoni.
[28] Iwo anapita ku Ofiri ndipo anakatenga golide okwana makilogalamu
14,000, amene anamupereka kwa Mfumu Solomoni.

# 10

### *Mfumu Yayikazi ya ku Seba Ibwera Kudzacheza ndi Solomoni*

[1] Mfumu yayikazi ya ku Seba itamva za kutchuka kwa Solomoni ndi za ubale wake ndi Yehova, inabwera kudzamuyesa ndi mafunso
okhwima. [2] Inafika mu Yerusalemu ndi gulu lalikulu la ngamira zonyamula zokometsera zakudya, golide wambiri ndi miyala yokongola.

Inafika kwa Solomoni ndipo inayankhula naye zonse zimene zinali mu
mtima mwake. 3 Solomoni anayankha mafunso ake onse ndipo panalibe
kanthu kalikonse kovuta komwe sanathe kufotokozera mfumu yayikaziyo.
4 Mfumu yayikazi ya ku Seba itaona nzeru zonse za Solomoni ndiponso
nyumba yaufumu imene anamanga, 5 chakudya cha pa tebulo pake, moyo
wa antchito ake ndi zovala zawo, atumiki opereka zakumwa, ndiponso
nsembe zopsereza zimene ankapereka ku Nyumba ya Yehova, inathedwa
nzeru.
6 Iyo inati kwa mfumu, "Mbiri imene ndinamva ndili ku dziko kwathu
ya zomwe munachita komanso nzeru zanu ndi yoona. 7 Koma sind-
inakhulupirire zinthu zimenezo mpaka nditafika ndi kuona ndi maso
anga. Kunena zoona sanandiwuze ngakhale theka lomwe, pakuti nzeru
ndi chuma zimene muli nazo zaposa zimene ndinamva. 8 Ngodala anthu
anu! Ngodala atumiki anu amene amayimirira pamaso panu nthawi
zonse ndi kumamva nzeru zanu! 9 Atamandike Yehova Mulungu wanu
amene wakondwera nanu nakukhazikani pa mpando waufumu wa Israeli.
Chifukwa cha chikondi chake chamuyaya pa Israeli, wayika inu kuti
mukhale mfumu kuti mulamulire moyenera ndi mwachilungamo."
10 Ndipo mfumu yayikaziyo inapatsa Solomoni golide wolemera mak-
ilogalamu 4,000, zokometsera zakudya zambirimbiri, ndiponso miyala
yokongola. Sikunabwerenso zokometsera zakudya ngati zomwe mfumu
yayikazi ya ku Seba inapatsa Mfumu Solomoni.
11 (Ndiponso sitima zapamadzi za Hiramu zinabweretsa golide wochok-
era ku Ofiri. Ndipo kuchokera kumeneko kunabweranso mitengo yambiri
ya alimugi ndi miyala yokongola. 12 Mfumu inagwiritsa ntchito mitengo
ya alimugi ngati yochirikizira Nyumba ya Yehova ndi nyumba yaufumu,
ndipo anapangiranso azeze ndi apangwe a anthu oyimba. Mitengo yotere
sinayitanitsidweponso kapena kuoneka mpaka lero lino).
13 Mfumu Solomoni inapereka kwa mfumu yayikazi ya ku Seba zonse
zimene inazifuna ndi kuzipempha, osawerengera mphatso zaufumu
zimene anali atamupatsa. Choncho inabwerera ku dziko la kwawo
pamodzi ndi atumiki ake.

### *Chuma ndi Ulemerero wa Solomoni*

14 Golide amene Solomoni ankalandira pa chaka ankalemera makilo-
galamu 23,000, 15 osawerengera misonkho imene anthu odzacheza ndi
amalonda amapereka. Golide wina ankachokera kwa mafumu onse a ku
Arabiya ndi kwa abwanamkubwa a m'dzikomo.
16 Mfumu Solomoni anapanga zishango zikuluzikulu 200 zagolide. Chis-
hango chilichonse chimapangidwa ndi golide wolemera makilogalamu
atatu ndi theka. 17 Anapanganso zishango zing'onozing'ono 300 zagolide.
Chishango chilichonse chimapangidwa ndi golide wolemera kilogalamu
imodzi ndi theka. Ndipo mfumu inayika zishangozo m'nyumba yake
yotchedwa Nyumba ya Nkhalango ya Lebanoni.
18 Mfumu inapangitsanso mpando waufumu waukulu wa minyanga ya
njovu, ndipo inawukutira ndi golide wabwino kwambiri. 19 Mpando wau-
fumuwo unali ndi makwerero asanu ndi limodzi, ndipo chotsamira chake
chinali chozungulira pamwamba pake. M'mbali zonse za mpandowo
munali zosanjikapo manja, pamodzi ndi chifaniziro cha mkango mbali
iliyonse. 20 Mikango khumi ndi iwiri inayimirira pa makwerero asanu
ndi limodziwo; mkango umodzi mbali iliyonse ya makwererowa. Mpando

woterewu sunapangidwepo mu ufumu wina uliwonse. 21 Zomwera zonse
za Mfumu Solomoni zinali zagolide, ziwiya zonse za Nyumba Yaufumu
ya Nkhalango ya Lebanoni zinali zagolide weniweni. Panalibe chimene
chinapangidwa ndi siliva chifukwa siliva sankayesedwa kanthu pa nthawi
ya Solomoni. 22 Mfumu inali ndi sitima zapamadzi zomwe zinali pa nyanja
pamodzi ndi sitima za Hiramu. Kamodzi pakapita zaka zitatu zinkabwera
zitanyamula golide, siliva ndi minyanga ya njovu, anyani ndi apusi.

23 Mfumu Solomoni inali yopambana pa chuma ndi pa nzeru kuposa
mafumu ena onse pa dziko lapansi. 24 Anthu onse a dziko lapansi
ankafunafuna kuyankhulana ndi Solomoni kuti amve nzeru zimene
Mulungu anayika mu mtima mwake. 25 Chaka ndi chaka aliyense amene
amabwera ankabweretsa mphatso za siliva ndi golide, mikanjo, zida
zankhondo ndi zokometsera zakudya, akavalo ndi abulu.

26 Solomoni anasonkhanitsa magaleta ndi akavalo; anali ndi magaleta
1,400 ndiponso oyendetsa akavalo 12,000, zimene anazisunga m'mizinda
ya magaleta ndiponso mu Yerusalemu. 27 Mfumu inachititsa kuti siliva
akhale ngati miyala wamba mu Yerusalemu, ndipo mkungudza unali
wochuluka ngati mitengo ya mkuyu ya m'mbali mwa phiri. 28 Akavalo a
Solomoni ankachokera ku Igupto komanso ku Kuwe. Anthu a malonda a
mfumu ankatengera akavalowo ku Kuwe. 29 Ankagula magaleta ku Igupto
pa mtengo wa masekeli asiliva okwana 600, ndipo akavalo pa mtengo wa
masekeli 150. Anthu amalondawo ankagulitsa zimenezi kwa mafumu onse
a Ahiti ndi Asiriya.

# 11

*Akazi a Solomoni*

1 Komatu Mfumu Solomoni anakonda akazi ambiri achilendo ndipo
kuwonjezera pa mwana wamkazi wa Farao, analinso ndi akazi a mi-
tundu iyi: Amowabu, Aamoni, Aedomu, Asidoni, ndi Ahiti. 2 Akazi
amenewa anali ochokera ku mitundu ija imene Yehova anawuza Aisraeli
kuti, "Simuyenera kudzakwatirana nawo amenewa, chifukwa ndithu,
amenewa adzatembenuza mitima yanu kuti mutsatire milungu yawo."
Komabe Solomoni anawakonda kwambiri akazi amenewa. 3 Iye anali
ndi akazi 700 ochokera ku mabanja achifumu ndi azikazi 300 ndipo
akaziwo anamusocheretsa. 4 Solomoni atakalamba, akazi akewo anakopa
mtima wake kuti atsatire milungu ina, ndipo sanatsatire Yehova Mulungu
wake ndi mtima wodzipereka, monga unalili mtima wa Davide abambo
ake. 5 Pakuti iye ankapembedza Asitoreti, mulungu wamkazi wa Asidoni,
ndiponso Moleki mulungu wonyansa wa Aamoni. 6 Kotero Solomoni
anachita zoyipa pamaso pa Yehova. Sanatsatire Yehova kwathunthu
monga anachitira Davide abambo ake.

7 Pa phiri la kummawa kwa Yerusalemu, anamanga malo opembedzer-
apo Kemosi, mulungu wonyansa wa Mowabu, ndiponso malo a Moleki,
mulungu wonyansa wa Aamoni. 8 Iye anamangiranso malo oterewa akazi
ake onse achilendo, amene amafukiza lubani ndi kumapereka nsembe
kwa milungu yawo.

9 Choncho Yehova anakwiyira Solomoni chifukwa mtima wake unatem-
benuka kuchoka kwa Yehova Mulungu wa Israeli, amene anamuonekera
kawiri konse. 10 Ngakhale kuti Yehova anamuletsa Solomoni kutsatira
milungu ina, iyeyo sanamvere lamulo la Yehova. 11 Pamenepo Yehova
anati kwa Solomoni, "Popeza mtima wako ndi wotere ndipo sunasunge

pangano langa ndi malamulo anga amene ndinakuwuza, ndithudi, Ine
ndidzawugawa ufumuwu kuwuchotsa kwa iwe ndi kuwupereka kwa
mmodzi mwa atumiki ako. 12 Koma chifukwa cha Davide abambo ako,
sindidzachita zimenezi iwe uli moyo. Ndidzawugawa m'dzanja la mwana
wako. 13 Komabe sindidzamulanda ufumu wonse, koma ndidzamusiyira
fuko limodzi chifukwa cha mtumiki wanga Davide ndiponso chifukwa cha
Yerusalemu, mzinda umene ndinawusankha."

### *Adani a Solomoni*

14 Ndipo Yehova anamuutsira Solomoni mdani, Hadadi Mwedomu,
wochokera ku banja laufumu ku Edomu. 15 Kale pamene Davide ankachita
nkhondo ndi Aedomu, Yowabu mkulu wa ankhondo, amene anapita
kukakwirira Aisraeli akufa, anakantha amuna onse ku Edomu. 16 Yowabu
ndi Aisraeli onse anakhala kumeneko miyezi isanu ndi umodzi mpaka
anawononga amuna onse a ku Edomu. 17 Koma Hadadi akanali mwana
anathawira ku Igupto pamodzi ndi akuluakulu ena a ku Edomu amene
ankatumikira abambo ake. 18 Iwo ananyamuka ku Midiya ndi kupita ku
Parani. Ndipo anatenga amuna ena ku Paraniko, napita nawo ku Igupto,
kwa Farao mfumu ya Igupto, amene anamupatsa nyumba, malo ndiponso
chakudya.

19 Farao anamukomera mtima Hadadi ndipo anamupatsa mkazi amene
anali mng'ono wake wa Mfumukazi Tahipenesi. 20 Mng'ono wake wa
Tahipenesi anabereka mwana wamwamuna ndipo anamutcha Genubati,
amene analeredwa m'nyumba yaufumu ndi Tahipenesi. Genubatiyo
ankakhala limodzi ndi ana a Farao.

21 Ali ku Iguptoko, Hadadi anamva kuti Davide ndi Yowabu anamwalira.
Pamenepo Hadadi anati kwa Farao, "Loleni ndichoke kuti ndibwerere ku
dziko la kwathu."

22 Farao anafunsa kuti, "Kodi ukusowa chiyani kuno kuti ufune
kubwerera ku dziko la kwanu?"

Hadadi anayankha kuti, "Palibe chimene ndikusowa, koma loleni kuti
ndichoke!"

23 Ndipo Mulungu anawutsira Solomoni mdani wina, Rezoni mwana
wa Eliada, amene anali atathawa mbuye wake, Hadadezeri mfumu ya
ku Zoba. 24 Iye anasonkhanitsa anthu ndipo anali mtsogoleri wa anthu
owukira pamene Davide anapha ankhondo a ku Zoba. Anthu owukirawa
anapita ku Damasiko, nakakhala kumeneko ndi kuyamba kulamulira.
25 Rezoni anali mdani wa Israeli pa masiku onse a Solomoni, kuwonjezera
pa mavuto amene ankabweretsa Hadadi. Kotero Rezoni ankalamulira ku
Aramu ndipo ankadana ndi Israeli.

### *Yeroboamu Awukira Solomoni*

26 Yeroboamu, mwana wa Nebati anawukiranso mfumu. Iye anali
mmodzi mwa akuluakulu a Solomoni wa fuko la Efereimu, wa ku Zeredi,
ndipo amayi ake anali Zeruya, mkazi wamasiye.

27 Nkhani ya kuwukira kwa Yeroboamu inali yotere: Solomoni ana-
manga malo a chitetezo a Milo ndipo anakonza khoma logumuka
la mzinda wa Davide, abambo ake. 28 Tsono Yeroboamu anali
munthu wamphamvu kwambiri ndipo Solomoni ataona kuti mnyamatayo
amadziwa kugwira ntchito bwino, anamuyika kukhala woyang'anira
anthu a ntchito onse a nyumba ya Yosefe.

29 Tsiku lina Yeroboamu ali pa ulendo kuchokera ku Yerusalemu, anaku-
mana ndi mneneri Ahiya pa msewu, ndipo Ahiyayo anali atavala mwinjiro

watsopano. Awiriwo anali okha kuthengoko, 30 ndipo Ahiya anagwira
mwinjiro watsopano umene anavala ndi kuwung'amba zidutswa 12.
31 Tsono iye anati kwa Yeroboamu, "Tenga zidutswa khumi, pakuti Yehova
Mulungu wa Israeli akuti, 'Taona, Ine ndidzachotsa ufumu m'dzanja la
Solomoni ndipo ndidzakupatsa iwe mafuko khumi. 32 Koma chifukwa
cha mtumiki wanga Davide ndiponso mzinda wa Yerusalemu, umene
ndinawusankha pakati pa mafuko a Israeli, iye adzakhala ndi fuko limodzi
lokha. 33 Ndidzachita zimenezi chifukwa wandisiya Ine ndi kupembedza
Asitoreti mulungu wamkazi wa Asidoni, Kemosi mulungu wa Amowabu
ndiponso Moleki mulungu wa Aamoni, ndipo sanayende m'njira yanga,
kapena kusunga mawu anga ndi malamulo anga monga anachitira Davide
abambo ake.

34 " 'Koma sindidzalanda ufumu wonse m'dzanja la Solomoni. Ine
ndamuyika kukhala wolamulira masiku onse a moyo wake chifukwa
cha mtumiki wanga Davide, amene ndinamusankha ndiponso amene
anamvera malamulo anga ndi mawu anga. 35 Ndidzalanda ufumu
m'dzanja la mwana wake ndipo ndidzakupatsa iwe mafuko khumi.
36 Ndidzapereka fuko limodzi kwa mwana wake ndi cholinga choti
Davide mtumiki wanga adzakhale nyale nthawi zonse pamaso panga
mu Yerusalemu, mzinda umene ndinawusankha kuyikamo Dzina langa.
37 Koma kunena za iwe, ndidzakutenga ndipo udzalamulira chilichonse
chimene mtima wako ukukhumba; udzakhala mfumu ya Israeli. 38 Ngati
udzamvera zonse zimene ndidzakulamula ndi kuyenda m'njira yanga ndi
kuchita zabwino pamaso panga, posunga malamulo anga ndi mawu anga
monga anachitira Davide mtumiki wanga, Ine ndidzakhala nawe. Ndidza-
kupatsa ufumu umene udzakhala wokhazikika monga ndinamupatsira
Davide, ndipo Ine ndidzakupatsa Israeli. 39 Ine ndidzalanga zidzukulu za
Davide chifukwa cha zimenezi, koma osati kwamuyaya.' "

40 Solomoni anafunitsitsa kupha Yeroboamu, koma Yeroboamu
anathawira ku Igupto, kwa Sisaki mfumu ya Igupto ndipo anakhala
kumeneko mpaka Solomoni atamwalira.

*Kumwalira kwa Solomoni*

41 Ntchito zina za Solomoni, zonse zomwe anachita komanso za nzeru
zake, kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya Solomoni? 42 Solomoni
analamulira Aisraeli onse mu Yerusalemu kwa zaka makumi anayi.
43 Ndipo anagona ndi makolo ake nayikidwa m'manda mu mzinda wa
Davide abambo ake. Ndipo Rehobowamu mwana wake analowa ufumu
m'malo ake.

# 12

*Aisraeli Awukira Rehobowamu*

1 Rehobowamu anapita ku Sekemu, pakuti Aisraeli onse n'kuti atapita
kumeneko kukamulonga ufumu. 2 Yeroboamu mwana wa Nebati anamva
zimenezi. Nthawi imeneyo n'kuti Yeroboamuyo akukhala ku Igupto,
pakuti atathawa Mfumu Solomoni iyeyo anakakhala ku Igupto. 3 Tsono
anthu anayitanitsa Yeroboamu, ndipo iye pamodzi ndi gulu lonse la ku
Israeli anapita kwa Rehobowamu ndipo anamuwuza kuti, 4 "Abambo
anu anatisenzetsa goli lolemetsa kwambiri, koma inu chepetsani ntchito
yowawa pa ife ndipo peputsani goli lolemetsa limene anatisenzetsa.
Mukatero tidzakutumikirani."

5 Rehobowamu anayankha kuti, “Pitani, ndipo pakatha masiku atatu, mudzabwerenso.” Choncho anthuwo anapitadi.

6 Ndipo Mfumu Rehobowamu anapempha nzeru kwa akuluakulu amene ankatumikira Solomoni abambo ake pamene anali ndi moyo. Iye anawafunsa kuti, “Kodi mungandilangize zotani kuti ndiwayankhe anthu amenewa?”

7 Iwo anayankha kuti, “Ngati lero mudzakhala mtumiki wa anthu amenewa ndi kuwatumikira ndipo mukawayankha bwino, iwowo adzakhala atumiki anu nthawi zonse.”

8 Koma Rehobowamu anakana malangizo amene akuluakuluwo anamupatsa ndipo anafunsira nzeru kwa anyamata anzake amene anakulira
nawo limodzi omwe ankamutumikira. 9 Iye anawafunsa kuti, “Kodi
malangizo anu ngotani? Kodi ndiwayankhe chiyani anthu amene akunena kwa ine kuti, ‘Peputsani goli limene abambo anu anatisenzetsa’?”

10 Anyamata anzake amene anakula nawo limodzi aja anamuyankha kuti, “Anthu amene ananena kwa iwe kuti, ‘Abambo anu anatisenzetsa goli lolemetsa, koma inu peputsani goli lathu,’ uwawuze kuti ‘Chala changa chakanise n’chachikulu kupambana chiwuno cha abambo anga.
11 Abambo anga ankakusenzetsani goli lolemetsa koma ine ndidzachititsa kuti likhale lolemera kwambiri. Abambo anga ankakukwapulani ndi zikoti wamba koma ine ndidzakukwapulani ndi zinkhanira.’ ”

12 Patapita masiku atatu, Yeroboamu pamodzi ndi anthu onse anabwera kwa Rehobowamu, monga momwe inanenera mfumu kuti, “Mudzabwere
pakatha masiku atatu.” 13 Mfumuyo inawayankha anthuwo mwankhanza.
Kukana malangizo amene akuluakulu anayipatsa. 14 Anatsatira malangizo amene anyamata anzake anamupatsa ndipo anati “Abambo anga ankakusenzetsani goli lolemetsa. Ine ndidzachititsa kuti likhale lolemera kwambiri. Abambo anga ankakukwapulani ndi zikoti wamba koma
ine ndidzakukwapulani ndi zinkhanira.” 15 Choncho mfumu sinamvere
pempho la anthuwo, pakuti zinthu izi zinali zochokera kwa Yehova, kukwaniritsa mawu amene Yehova anayankhula kwa Yeroboamu mwana wa Nebati kudzera mwa Ahiya wa ku Silo.

16 Aisraeli onse ataona kuti mfumu yakana kumva zopempha zawo, iwo anayankha mfumu kuti,

“Kodi ife tili ndi gawo lanji mwa Davide,
ndi gawo lanjinso mwa mwana wa Yese?
Inu Aisraeli, bwererani ku matenti anu!
Ziyang’anira nyumba yako, Iwe Davide!”

Kotero Aisraeli anachoka napita ku nyumba zawo. 17 Koma Aisraeli amene
ankakhala m’mizinda ya Yuda ankalamuliridwa ndi Rehobowamu.

18 Mfumu Rehobowamu anatuma Adoramu amene ankayang’anira ntchito yathangata, koma Aisraeli onse anamugeda ndi miyala mpaka kumupha. Koma Mfumu Rehobowamu anakwera msangamsanga galeta
wake nathawira ku Yerusalemu. 19 Choncho Aisraeli akhala akuwukira
nyumba ya Davide mpaka lero lino.

20 Aisraeli onse atamva kuti Yeroboamu wabwerera kuchokera ku Igupto, anatumiza mawu okamuyitana kuti abwere ku msonkhano ndipo anamuyika kukhala mfumu ya Aisraeli onse. Fuko la Yuda lokha ndi lomwe linkatsatira nyumba ya Davide.

21 Rehobowamu atafika ku Yerusalemu, anasonkhanitsa nyumba yonse ya Yuda ndi fuko la Benjamini, nasankha ankhondo okwanira 180,000,

kuti akamenyane ndi nyumba ya Israeli kuti amubwezere Rehobowamu
mwana wa Solomoni ufumu wake.
22 Koma Mulungu anayankhula ndi Semaya, munthu wa Mulungu kuti,
23 "Nena kwa Rehobowamu mwana wa Solomoni mfumu ya Yuda, kwa
nyumba yonse ya Yuda ndi Benjamini, ndiponso kwa anthu ena onse
kuti, 24 'Yehova akuti: Musapite kukamenyana ndi abale anu Aisraeli.
Aliyense wa inu abwerere kwawo, pakuti zimenezi ndachita ndine.' "
Choncho anthuwo anamvera mawu a Yehova ndi kubwerera kwawo,
monga analamulira Yehova.

### *Mafano a Golide a Ana Ang'ombe ku Beteli ndi ku Dani*

25 Tsono Yeroboamu anamanga mzinda wa Sekemu m'dziko la mapiri
la Efereimu ndipo anakhala kumeneko. Kuchokera kumeneko anapita
kukamanga mzinda wa Penueli.
26 Yeroboamu anaganiza mu mtima mwake kuti, "Ndithu, ufumuwu
udzabwereranso ku nyumba ya Davide. 27 Ngati anthuwa azipitabe
kukapereka nsembe ku Nyumba ya Yehova ku Yerusalemu, adzayambanso
kutsatira mbuye wawo Rehobowamu, mfumu ya Yuda. Adzandipha ndi
kubwerera kwa Mfumu Rehobowamu."
28 Itapempha nzeru, mfumuyo inapanga mafano awiri a ana ang'ombe.
Mfumuyo inati kwa anthuwo, "Mwakhala mukupita ku Yerusalemu
nthawi yayitali. Iwe Israeli, nayi milungu yako imene inakutulutsa
m'dziko la Igupto." 29 Fano lina analiyika ku Beteli ndipo lina analiyika
ku Dani. 30 Ndipo zimenezi zinachimwitsa anthu pakuti anthu ankapita
mpaka ku Dani kukapembedza fano limene linali kumeneko.
31 Yeroboamu anamanga Nyumba za Mulungu pa malo azipembedzo
nasankha ansembe kuchokera pakati pa anthu wamba, ngakhale sanali
Alevi. 32 Iye anakhazikitsa chikondwerero pa tsiku la 15 la mwezi
wachisanu ndi chitatu, lofanana ndi tsiku la chikondwerero cha ku
Yuda, ndipo ankapereka nsembe pa guwa. Izi ankachita ku Beteli,
kupereka nsembe kwa ana ang'ombe amene anapanga. Ndipo ku Beteliko
anayikako ansembe pa malo achipembedzo amene anamanga. 33 Tsiku
la 15 la mwezi wachisanu ndi chitatu, mwezi umene anawusankha
yekha, anapereka nsembe pa guwa limene analimanga ku Beteli. Motero
anakhazikitsa chikondwerero cha Aisraeli ndipo iye ankapita kukapereka
nsembe yofukiza lubani pa guwa.

# 13

### *Munthu wa Mulungu Wochokera ku Yuda*

1 Ndipo taonani, munthu wa Mulungu wochokera ku Yuda anapita ku
Beteli molamulidwa ndi Yehova. Nthawi imeneyo n'kuti Yeroboamu atay-
imirira pambali pa guwa akufukiza lubani. 2 Mneneriyo anatemberera
guwalo mofuwula potsata mawu a Yehova nati: "Guwa iwe, guwa iwe!
Yehova akuti, 'Taonani m'banja la Davide mudzabadwa mwana dzina lake
Yosiya. Pa iwe, iyeyo adzaperekapo ngati nsembe, ansembe otumikira ku
malo achipembedzo amene tsopano akufukiza lubani pa iwe, ndipo pa iwe
adzatenthapo mafupa a anthu.' " 3 Tsiku lomwelo munthu wa Mulungu uja
anapereka chizindikiro ichi: "Chizindikiro chimene Yehova wanena ndi
ichi: Taonani guwali lidzang'ambika pakati ndipo phulusa lili pamenepo
lidzamwazika."

4 Mfumu Yeroboamu atamva zimene munthu wa Mulungu ananena
motemberera guwa lansembe ku Beteli, anatambasula dzanja lake ali ku
guwako ndipo anati, “Mugwireni!” Koma dzanja limene anatambasula ku-
loza munthu wa Mulunguyo linawuma kuti gwaa, kotero kuti sanathenso
kulibweza. 5 Nthawi yomweyo guwa lija linang’ambika pakati ndipo
phulusa lake linamwazika molingana ndi chizindikiro chimene munthu
wa Mulungu anapereka potsata mawu a Yehova.

6 Pamenepo mfumu inati kwa munthu wa Mulunguyo, “Undipem-
pherere kwa Yehova Mulungu wako kuti andikomere mtima ndipo
undipempherere kuti dzanja langa lichire.” Choncho munthu wa Mu-
lungu anapempha kwa Yehova, ndipo dzanja la mfumu linachiritsidwa
n’kukhala ngati momwe linalili kale.

7 Mfumu inati kwa munthu wa Mulunguyo, “Tiye kwathu kuti ukadye
chakudya, ndipo ndidzakupatsa mphatso.”

8 Koma munthu wa Mulunguyo anayankha mfumu kuti, “Ngakhale
mutandipatsa theka la chuma chanu, sindingapite nanu, kapena kudya
chakudya, kapenanso kumwa madzi kuno. 9 Pakuti Yehova anandilamula
kuti, ‘Usakadye chakudya kapena kumwa madzi kapena kubwerera podz-
era njira imene unayendamo kale.’ ” 10 Choncho munthu wa Mulunguyo
anadzera njira ina ndipo sanatsate njira imene anayendamo pobwera ku
Beteliko.

11 Tsono ku Beteli kunkakhala mneneri wina wokalamba. Mmodzi mwa
ana ake anamufotokozera zonse zomwe munthu wa Mulungu anachita
kumeneko tsiku limenelo. Anawuzanso abambo ake zimene ananena
kwa mfumu. 12 Abambo awo aja anawafunsa kuti, “Kodi wadzera njira
iti?” Ana akewo anamufotokozera njira imene munthu wa Mulungu
wochokera ku Yudayo anadzera. 13 Ndipo abambo aja anati kwa ana
akewo, “Mangireni chishalo pa bulu.” Anawo atamangirira chishalo pa
bulu, nkhalambayo inakwera buluyo 14 ndipo inalondola munthu wa
Mulunguyo. Inamupeza atakhala pansi pa mtengo wa thundu ndipo
inamufunsa kuti, “Kodi ndiwe munthu wa Mulungu amene anabwera
kuchokera ku Yuda?”

Munthuyo anayankha kuti, “Inde, ndineyo.”

15 Choncho mneneri wokalambayo anati kwa iye, “Tiye kwathu kuti
ukadye chakudya.”

16 Munthu wa Mulungu uja anati, “Sindingabwerere nanu kapena
kudya chakudya kapenanso kumwa madzi kuno. 17 Pakuti ndawuzidwa
ndi Yehova kuti, ‘Usadye chakudya kapena kumwa madzi kumeneko
kapenanso kubwerera poyenda njira imene unayendamo popita.’ ”

18 Mneneri wokalambayo anayankha kuti, “Inenso ndine mneneri ngati
iwe. Ndipo mngelo wa Yehova anayankhula nane mawu a Yehova kuti,
‘Kamubweze abwere ku nyumba yako kuti akadye chakudya ndi kumwa
madzi.’ ” Koma anamunamiza. 19 Choncho munthu wa Mulungu uja
anabwerera naye ndipo anakadya ndi kumwa madzi m’nyumba mwake.

20 Ali pa tebulo, Yehova anayankhula ndi mneneri wokalambayo amene
anamubweza munthu wa Mulunguyo. 21 Iye anafuwulira munthu wa
Mulungu wochokera ku Yudayo kuti, “Yehova akuti, ‘Iwe wanyoza
mawu a Yehova ndipo sunasunge lamulo limene Yehova Mulungu wako
anakupatsa. 22 Iwe wabwerera ndi kudya chakudya ndiponso kumwa
madzi ku malo amene Iye anakuwuza kuti usadye chakudya kapena
kumwa madzi. Choncho mtembo wako sadzawuyika m’manda a makolo
ako.’ ”

[23] Munthu wa Mulungu atatha kudya ndi kumwa, mneneri amene
anamubweza uja anamangirira chishalo pa bulu wa munthu wa Mulun-
guyo. [24] Akupita, anakumana ndi mkango pa msewu ndipo unamupha,
mtembo wake unagwera pansi pa msewu, bulu uja anayima pambali pake
ndipo mkango unayima pafupi ndi mtembowo. [25] Ndipo taonani, anthu
ena amene ankapita mu msewumo anaona mtembowo uli pansi potero,
mkango utayima pa mbali pa mtembo uja ndipo anapita nakafotokozera
anthu mu mzinda umene mumakhala mneneri wokalamba uja.
[26] Mneneri amene anamubweza mnzake ku njira uja atamva zimenezi,
anati, "Ameneyo ndi munthu wa Mulungu amene wanyoza mawu a
Yehova. Yehova wamupereka kwa mkango umene wamukhadzula ndi
kumupha, monga momwe Yehova anamuchenjezera."
[27] Mneneri wokalambayo anati kwa ana ake, "Mundimangire chishalo
pa bulu," ndipo anaterodi. [28] Ndipo anapita, nakapezadi mtembo
utagwera pansi mu msewu, bulu pamodzi ndi mkango atayima pambali
pake. Koma mkangowo sunadye mtembowo kapena kukhadzula buluyo.
[29] Choncho mneneri wokalambayo anatenga mtembo wa munthu wa
Mulunguyo, nawuyika pa bulu, ndipo anabwera nawo ku mzinda kuti
alire maliro ndi kuyika mtembowo m'manda. [30] Tsono anayika mtem-
bowo m'manda amene mneneri wokalamba uja anadzikonzera, ndipo
anamulira pomanena kuti, "M'bale wanga ine! M'bale wanga ine!"
[31] Atamuyika m'manda, iye anati kwa ana ake, "Ine ndikafa,
mudzandiyike m'manda amene munthu wa Mulungu wayikidwa. Mudza-
yike mafupa anga pambali pa mafupa ake. [32] Pakuti uthenga umene
Yehova anamuyankhulitsa, wotsutsana ndi guwa lansembe la ku Beteli ndi
nyumba zonse za chipembedzo za m'mizinda ya ku Samariya, zidzachitika
ndithu."
[33] Ngakhale izi zinachitika, Yeroboamu sanasiye njira zake zoyipa, koma
anasankhanso anthu wamba kukhala ansembe pa malo ake achipem-
bedzo. Aliyense amene ankafuna kukhala wansembe iye anamupatula
kukhala wansembe. [34] Limeneli ndiye linali tchimo la nyumba ya
Yeroboamu limene linabweretsa kugwa kwake ndiponso chiwonongeko
m'dzikomo.

# 14

### *Ahiya Anenera za Kugwa kwa Yeroboamu*

[1] Pa nthawi imeneyo Abiya mwana wa Yeroboamu anayamba kudwala,
[2] ndipo Yeroboamu anati kwa mkazi wake, "Nyamuka ndipo udzibise
kuti usadziwike kuti ndiwe mkazi wa Yeroboamu, ndipo upite ku Silo.
Kumeneko kuli mneneri Ahiya amene anandiwuza kuti ndidzakhala
mfumu ya anthu awa. [3] Utenge buledi khumi, makeke ndiponso
botolo la uchi ndipo upite kwa mneneriyo. Iye adzakuwuza zimene
zidzamuchitikire mwanayu." [4] Choncho mkazi wa Yeroboamu anadzibisa
ndipo anapita ku nyumba ya Ahiya ku Silo.
Tsono Ahiya sankatha kupenya bwino. Ankangoona kuti mbuu chi-
fukwa cha ukalamba. [5] Koma Yehova n'kuti atamuwuza Ahiya kuti,
"Taona, mkazi wa Yeroboamu akubwera kudzafunsa iwe za mwana wake
pakuti akudwala, ndiye udzamuyankhe zakutizakuti mkaziyo. Iye akafika,
adzadzibisa."
[6] Tsono Ahiya atamva mgugu wa mapazi ake pa khomo, anati, "Lowa,
iwe mkazi wa Yeroboamu. Bwanji ukudzibisa? Ine ndatumidwa kuti
ndikuwuze nkhani yoyipa. [7] Pita, kamuwuze Yeroboamu kuti Yehova

Mulungu wa Israeli akuti, 'Ine ndinakukweza pakati pa anthu ndipo
ndinakuyika kukhala mtsogoleri wa anthu anga Aisraeli. 8 Ndinachotsa
ufumu ku nyumba ya Davide ndi kuwupereka kwa iwe, koma iwe
sunafanane ndi mtumiki wanga Davide, amene ankasunga malamulo
anga ndi kunditsata Ine ndi mtima wake wonse, kuchita zolungama
zokhazokha pamaso panga. 9 Ndipo iwe wachita zoyipa kupambana onse
amene analipo kale. Wadzipangira milungu ina, mafano a zitsulo. Iweyo
wandikwiyitsa ndipo wandiwukira.

10 " 'Choncho taona, ndidzabweretsa masautso pa nyumba ya Yer-
oboamu. Ndipo ndidzawononga munthu wamwamuna aliyense wa
pa banja lako, kapolo pamodzi ndi mfulu yemwe m'dziko la Israeli.
Ndidzatentha nyumba ya Yeroboamu monga mmene munthu amatenthera
ndowe mpaka yonse kutheratu. 11 Agalu adzadya aliyense wa banja la
Yeroboamu amene adzafere mu mzinda, ndipo mbalame zamlengalenga
zidzadya iwo amene adzafere ku thengo, pakuti Yehova watero!'

12 "Ndipo iwe nyamuka, bwerera ku nyumba kwako. Phazi lako
likadzangoponda mu mzindamo, mwanayo adzamwalira. 13 Aisraeli onse
adzalira maliro ake ndi kumuyika m'manda. Ndi yekhayo wa banja la
Yeroboamu amene adzayikidwe m'manda, pakuti ndi mwa iye yekha
mmene Yehova Mulungu wa Israeli wapezamo kanthu kabwino.

14 "Koma Yehova adzadzisankhira yekha mfumu yolamulira Israeli
imene idzawononga banja la Yeroboamu. Tsiku lake ndi lero! Ndati
chiyani? Inde, ndi lero lomwe lino. 15 Ndipo Yehova adzakantha
Israeli, kotero kuti adzakhala ngati bango logwedera pa madzi. Iye
adzazula Israeli m'dziko labwino limene analipereka kwa makolo ake
ndi kuwamwazira kutsidya kwa mtsinje wa Yufurate, chifukwa anakwiy-
itsa Yehova pamene anapanga mafano a Asera. 16 Ndipo Iye sadza-
samalanso Israeli chifukwa cha machimo amene anachita Yeroboamu ndi
kuchimwitsa nawo Israeli."

17 Tsono mkazi wa Yeroboamu anayimirira nachoka kupita ku Tiriza.
Atangoponda pa khonde la nyumba yake, mwana uja anamwalira.
18 Aisraeli anamuyika m'manda, ndipo onse analira maliro ake, monga
momwe Yehova ananenera kudzera mwa mtumiki wake, mneneri Ahiya.

19 Ntchito zina pa nthawi ya ulamuliro wa Yeroboamu, nkhondo zake
ndi mmene ankalamulirira zinalembedwa m'buku la mbiri ya mafumu a
Israeli. 20 Iye analamulira zaka 22 ndipo anamwalira nayikidwa m'manda
pamodzi ndi makolo ake. Ndipo Nadabu mwana wake analowa ufumu
m'malo mwake.

### *Rehobowamu Mfumu ya Yuda*

21 Rehobowamu mwana wa Solomoni anali mfumu ya ku Yuda. Iye
analowa ufumu ali ndi zaka 41, ndipo analamulira zaka 17 ku Yerusalemu,
mzinda umene Yehova anawusankha pakati pa mafuko a Israeli kuti
ayikemo Dzina lake. Amayi ake anali Naama, wa ku Amoni.

22 Anthu a ku Yuda anachita zoyipa pamaso pa Yehova kupambana
mmene anachitira makolo awo ndipo Yehova anawakwiyira. 23 Iwonso
anadzipangira malo opembedzerapo mafano pa chitunda chilichonse
ndi kuyimika miyala ya chipembedzo ndi mitengo ya Asera pa mtengo
uliwonse wa masamba ambiri. 24 M'dzikomo munalinso amuna ochita
zachiwerewere mwa chipembedzo. Anthu ankachita zonyansa zonse za
anthu a mitundu ina imene Yehova anayipirikitsa asanafike Aisraeli.

25 Chaka chachisanu cha ufumu wa Rehobowamu, Sisaki, mfumu ya
Igupto, anadzathira nkhondo Yerusalemu. 26 Ananyamula chuma cha ku
Nyumba ya Yehova ndiponso chuma cha ku nyumba ya mfumu. Anatenga
chilichonse, ngakhalenso zishango zonse zagolide zimene Solomoni ana-
panga. 27 Ndipo Mfumu Rehobowamu anapanga zishango zamkuwa
m'malo mwake, nazipereka m'manja mwa olamulira alonda a pa khomo
pa nyumba ya mfumu. 28 Nthawi zonse mfumu ikamapita ku Nyumba ya
Yehova, alonda ankanyamula zishangozo, kenaka ankazisunga m'chipinda
cha alonda.
29 Tsono ntchito zina za Rehobowamu ndi zina zonse zimene anachita,
kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 30 Panali
nkhondo zosalekeza pakati pa Rehobowamu ndi Yeroboamu. 31 Ndipo
Rehobowamu anamwalira nayikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake
mu mzinda wa Davide. Amayi ake anali Naama wa ku Amoni. Ndipo
Abiya analowa ufumu m'malo mwa abambo ake.

# 15

*Abiya Mfumu ya Yuda*

1 M'chaka cha 18 cha ulamuliro wa Yeroboamu mwana wa Nebati, Abiya
anakhala mfumu ya Yuda, 2 ndipo analamulira mu Yerusalemu zaka zitatu.
Amayi ake anali Maaka, mwana wa Abisalomu.
3 Abiya anachita zoyipa zonse zimene abambo ake anazichita. Sanali
wangwiro pamaso pa Yehova Mulungu wake, monga linachitira kholo lake
Davide. 4 Komabe chifukwa cha Davide, Yehova Mulungu wake anamu-
patsa nyale mu Yerusalemu pomupatsa mwana wolowa m'malo mwake
ndi kumukhazikitsa kukhala wamphamvu mu Yerusalemu; 5 pakuti Da-
vide anachita zolungama pamaso pa Yehova ndipo sanalephere kusunga
chilichonse chimene Yehova anamulamula masiku onse a moyo wake
kupatula nkhani ija ya Uriya Mhiti.
6 Panali nkhondo pakati pa Rehobowamu ndi Yeroboamu masiku onse
a moyo wa Abiya. 7 Tsono ntchito zina za Abiya, ndi zina zonse anachita,
kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? Panali nkhondo
pakati pa Abiya ndi Yeroboamu. 8 Ndipo Abiya anamwalira nayikidwa
m'manda momwe anayikidwa makolo ake mu Mzinda wa Davide. Ndipo
Asa, mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

*Asa Mfumu ya Yuda*

9 M'chaka cha makumi awiri cha Yeroboamu mfumu ya Israeli, Asa
anakhala mfumu ya Yuda, 10 ndipo analamulira mu Yerusalemu kwa zaka
41. Agogo ake akazi anali Maaka mwana wa Abisalomu.
11 Asa anachita zolungama pamaso pa Yehova monga anachitira Davide
kholo lake. 12 Iye anachotsa m'dzikomo amuna onse ochita zadama
pochita chipembedzo chawo ndiponso anachotsa mafano onse amene
makolo ake anawapanga. 13 Iye anachotsanso gogo wake Maaka pa
udindo wake wa amayi a mfumu, chifukwa choti anapanga fano lonyansa
la Asera. Asa anagwetsa fanolo nakalitentha ku Chigwa cha Kidroni.
14 Ngakhale sanachotse malo opembedzerapo mafano, mtima wa Asa
unali wodzipereka kwathunthu kwa Yehova masiku onse a moyo wake.
15 Asa anabweretsa ku Nyumba ya Yehova zinthu zimene abambo ake
anazipereka, ndiponso zinthu zimene iye mwini anazipereka: zagolide,
siliva ndi ziwiya zotengera.

16 Panali nkhondo pakati pa Asa ndi Baasa mfumu ya Israeli nthawi
yonse ya ulamuliro wawo. 17 Baasa mfumu ya Israeli anapita kukathira
nkhondo dziko la Yuda, ndipo anamangira linga mzinda wa Rama kuletsa
kuti wina aliyense asatuluke kapena kulowa m'dziko la Asa, mfumu ya
Yuda.

18 Tsono Asa anatenga siliva yense pamodzi ndi golide zimene zinatsala
ku malo osungira chuma cha ku Nyumba ya Yehova ndiponso ku nyumba
yake yaufumu. Anazipereka kwa atumiki ake, nawatuma kupita nazo
kwa Beni-Hadadi mwana wa Tabirimoni, mwana wa Heziyoni, mfumu
ya Aramu, amene ankakhala ku Damasiko ndipo anakamuwuza kuti,
19 "Tiyeni tigwirizane inu ndi ine, monga panali mgwirizano pakati pa
abambo anu ndi abambo anga. Onani, ndikukutumizirani mphatso za
siliva ndi golide. Tsopano kathetseni mgwirizano wanu ndi Baasa mfumu
ya Israeli kuti andisiye."

20 Choncho Beni-Hadadi anamvera zimene ananena mfumu Asa ndipo
anatumiza olamulira magulu ake ankhondo ku mizinda ya Israeli. Ndipo
iye anagonjetsa Iyoni, Dani, Abeli-Beti-Maaka ndi dera lonse la Kinereti
kuphatikiza dziko lonse la Nafutali. 21 Baasa atamva zimenezi, anasiya
kumangira linga Rama ndipo anakakhala ku Tiriza. 22 Pamenepo Mfumu
Asa analamula anthu onse a ku Yuda osasiya ndi mmodzi yemwe, ndipo
anachotsa ku Rama miyala ndi matabwa amene Baasa ankamangira
kumeneko. Zipangizo zimenezi Mfumu Asa inamangira linga la Geba ku
Benjamini ndi la ku Mizipa.

23 Tsono ntchito zina za Asa, za mphamvu zake ndi mizinda imene
anayimanga ndi zina zonse zimene anachita, kodi sizinalembedwe m'buku
la mbiri ya mafumu a Yuda? Koma pa nthawi ya ukalamba wake anadwala
nthenda ya mapazi. 24 Ndipo Asa anamwalira nayikidwa m'manda
momwe anayikidwa makolo ake mu mzinda wa Davide kholo lake. Ndipo
Yehosafati mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

### *Nadabu Mfumu ya Israeli*

25 Nadabu, mwana wa Yeroboamu anakhala mfumu ya Israeli m'chaka
chachiwiri cha Asa mfumu ya Yuda, ndipo analamulira Israeli zaka
ziwiri. 26 Nadabu anachita zoyipa pamaso pa Yehova, anayenda m'njira
za abambo ake ndi mu uchimo womwe anachimwitsa nawo Israeli.

27 Baasa mwana wa Ahiya, wa banja la Isakara anakonzera Nadabuyo
chiwembu, ndipo anamukantha ku Gibetoni, mzinda wa Afilisti, pamene
Nadabu ndi anthu onse a ku Israeli anali atawuzungulira. 28 Baasa anapha
Nadabu m'chaka chachitatu cha Asa, mfumu ya ku Yuda ndipo analowa
ufumu m'malo mwake.

29 Iye atangoyamba kulamulira, anapha anthu onse a banja la Yer-
oboamu. Sanasiye ndi mmodzi yemwe wamoyo pa banjapo, koma ana-
wononga anthu onse, molingana ndi mawu a Yehova amene anayankhula
mwa mtumiki wake Ahiya wa ku Silo 30 chifukwa cha machimo amene
Yeroboamu anachita, ndiponso kuchimwitsa anthu a ku Israeli, naputa
mkwiyo wa Yehova Mulungu wa Israeli.

31 Tsono ntchito za Nadabu ndi zina zonse zimene anazichita, kodi
sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli? 32 Panali nkhondo
pakati pa Asa ndi Baasa mfumu ya Israeli pa nthawi yonse ya ulamuliro
wawo.

### *Baasa Mfumu ya Israeli*

33 Chaka chachitatu cha Asa mfumu ya Yuda, Baasa mwana wa Ahiya
anakhala mfumu ya Aisraeli onse ku Tiriza, ndipo analamulira zaka 24.
34 Anachita zoyipa pamaso pa Yehova, nayenda m'njira za Yeroboamu ndi
kuchita tchimo lake limene linachimwitsa anthu a ku Israeli.

# 16

1 Ndipo Yehova anayankhula kudzera mwa Yehu mwana wa Hanani,
mawu odzudzula Baasa kuti, 2 "Ine ndinakukuza kuchokera pa fumbi
ndipo ndinakupanga kuti ukhale mtsogoleri wa anthu anga Aisraeli,
koma iwe wakhala ukuyenda m'njira za Yeroboamu ndi kuchimwitsa
anthu anga Aisraeli naputa mkwiyo wanga chifukwa cha machimo awo.
3 Taonani, Ine ndatsala pang'ono kuwononga Baasa pamodzi ndi nyumba
yake, ndipo ndidzachitira nyumba yake zimene ndinachita pa nyumba ya
Yeroboamu mwana wa Nebati. 4 Agalu adzadya aliyense wa banja la Baasa
amene adzafere mu mzinda, ndipo mbalame za mu mlengalenga zidzadya
iwo amene adzafere kuthengo."

5 Tsono ntchito zina za Baasa ndi zamphamvu zake zimene anachita,
kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli? 6 Baasa
anamwalira nayikidwa m'manda amene anayikidwa makolo ake ku Tiriza.
Ndipo Ela mwana wake anakhala mfumu m'malo mwake.

7 Komatu Yehova anayankhula kwa Baasa pamodzi ndi banja lake
lonse kudzera mwa mneneri Yehu mwana wa Hanani, chifukwa cha
zoyipa zonse zimene iye anachita pamaso pa Yehova, kukwiyitsa Yehovayo
nakhala ngati nyumba ya Yeroboamu ndiponso chifukwa anawonongeratu
banja la Yeroboamu.

### *Ela Mfumu ya Israeli*

8 M'chaka cha 26 cha ufumu wa Asa mfumu ya Yuda, Ela mwana wa
Baasa anakhala mfumu ya Israeli, ndipo analamulira ku Tiriza zaka ziwiri.

9 Zimuri, mmodzi mwa akuluakulu ake, amene ankalamulira theka
la magaleta ake, anamuchitira chiwembu. Nthawi imeneyi Ela anali
ku Tiriza, akumwa koledzera nako m'nyumba ya Ariza, munthu amene
ankayang'anira nyumba yaufumu ku Tiriza. 10 Zimuri anadzalowa,
namukantha ndi kumupha m'chaka cha 27 cha Asa mfumu ya Yuda. Ndipo
Zimuriyo anakhala mfumu m'malo mwake.

11 Zimuri atangoyamba kulamulira, anapha banja lonse la Baasa.
Sanasiyepo munthu wamwamuna ndi mmodzi yemwe, wachibale kapena
bwenzi lake. 12 Choncho Zimuri anawononga banja lonse la Baasa,
molingana ndi mawu amene Yehova anayankhula motsutsa Baasa kudzera
mwa mneneri Yehu, 13 chifukwa cha machimo onse amene Baasa ndi
mwana wake Ela anachita nachimwitsa Israeli, anakwiyitsa Yehova,
Mulungu wa Israeli ndi mafano awo osapindulitsa.

14 Tsono ntchito zina za Ela ndi zina zonse zimene anachita, kodi
sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli?

### *Zimuri Mfumu ya Israeli*

15 M'chaka cha 27 cha Asa mfumu ya Yuda, Zimuri analamulira ku Tiriza
masiku asanu ndi awiri. Gulu la ankhondo linali litamanga misasa pafupi
ndi Gibetoni, mzinda wa Afilisti. 16 Ankhondo amene anali ku misasa
atamva kuti Zimuri wachita chiwembu ndi kupha mfumu, tsiku lomwelo
ku misasako anasankha Omuri, mkulu wa ankhondo kukhala mfumu ya

Israeli. 17 Tsono Omuri ndi Aisraeli onse amene anali naye anachoka
ku Gibetoni ndi kukazinga Mzinda wa Tiriza. 18 Zimuri ataona kuti
mzinda walandidwa, anathawira ku nsanja ya nyumba ya mfumu ndipo
anatentha nyumbayo iye ali momwemo. Kotero iyeyo anafa, 19 chifukwa
cha machimo amene iye anachita, kuchita zoyipa pamaso pa Yehova ndi
kuyenda m'njira za Yeroboamu, nachimwitsa nazo Aisraeli.
20 Tsono ntchito zina za Zimuri ndi chiwembu chake chimene anachita,
kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli?

### *Omuri Mfumu ya Israeli*

21 Pambuyo pake Aisraeli anagawikana pakati: theka linatsatira Tibini
mwana wa Ginati kuti limulonge ufumu, ndipo theka lina linatsatira
Omuri. 22 Koma anthu otsatira Omuri anali amphamvu kupambana amene
ankatsatira Tibini mwana wa Ginati. Choncho Tibini anafa ndipo Omuri
anakhala mfumu.
23 M'chaka cha 31 cha Asa mfumu ya Yuda, Omuri anakhala mfumu
ya Israeli, ndipo analamulira zaka 12 ndi miyezi isanu ndi umodzi ku
Tiriza. 24 Iye anagula phiri la Samariya kwa Semeri pa mtengo wa ndalama
6,000 za siliva ndipo pa phiripo anamangapo mzinda, nawutcha Samariya,
potsata dzina la Semeri, dzina la mwini wakale wa phirilo.
25 Koma Omuri anachita zoyipa pamaso pa Yehova ndipo anachimwa
kuposa mafumu ena onse amene analipo iye asanakhale mfumu. 26 Pakuti
iye anayenda m'njira zonse za Yeroboamu mwana wa Nebati, ndipo
tchimo lake anachimwitsa nalo Aisraeli, nakwiyitsa Yehova Mulungu wa
Israeli ndi mafano awo opandapake.
27 Tsono ntchito zina za Omuri ndi zamphamvu zimene anachita, kodi
sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli? 28 Choncho
Omuri anamwalira nayikidwa m'manda amene anayikidwa makolo ake
ku Samariya. Ndipo Ahabu mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

### *Ahabu Akhala Mfumu ya Israeli*

29 M'chaka cha 38 cha ufumu wa Asa, mfumu ya Yuda, Ahabu mwana
wa Omuri anakhala mfumu ya Israeli nalamulira Israeli ku Samariya
zaka 22. 30 Ahabu mwana wa Omuri anachita zoyipa zambiri pamaso pa
Yehova kupambana mafumu onse akale. 31 Iye sanachiyese ngati chinthu
chochepa chabe kuchita machimo a Yeroboamu mwana wa Nebati, koma
anakwatiranso Yezebeli, mwana wa Etibaala mfumu ya Asidoni, nayamba
kutumikira Baala ndi kumupembedza. 32 Iye anapangira Baala guwa
lansembe m'nyumba ya Baala imene anamanga ku Samariya. 33 Ahabu
anapanganso fano la Asera ndi kukwiyitsa kwambiri Yehova Mulungu wa
Israeli, kupambana mafumu onse a Israeli amene analipo iye asanakhale
mfumu.
34 Pa nthawi ya Ahabu, Hiyeli wa ku Beteli anamanganso mzinda
wa Yeriko. Pa nthawi yomanga maziko ake, mwana wake woyamba
wa mwamuna, Abiramu anamwalira, ndipo pa nthawi yomanga zipata
zake, mwana wa mng'ono wa mwamuna Segubu, anamwaliranso. Izi
zinachitika monga momwe Yehova ananenera kudzera mwa Yoswa
mwana wa Nuni.

## 17

### *Makwangwala Adyetsa Eliya*

1 Ndipo mneneri Eliya wa ku Tisibe ku Giliyadi, anati kwa Ahabu,
“Pali Yehova wamoyo, Mulungu wa Israeli, amene ndimamutumikira,
sipadzakhala mame kapena mvula zaka zikubwerazi, pokhapokha ine
nditanena.”

2 Pamenepo Yehova anayankhula ndi Eliya kuti, 3 “Choka kuno, upite
kummawa, ukabisale m’mbali mwa mtsinje wa Keriti, pafupi ndi Yoro-
dani. 4 Uzikamwa mu mtsinjemo, ndipo ndalamula makwangwala kuti
azikakudyetsa kumeneko.”

5 Choncho Eliya anachita zomwe Yehova anamuwuza. Anapita
ku mtsinje wa Keriti, pafupi ndi Yorodani, nakakhala kumeneko.
6 Makwangwala ankabweretsera buledi ndi nyama mmawa ndi madzulo,
ndipo ankamwa mu mtsinjemo.

### *Mayi Wamasiye wa ku Zarefati*

7 Patapita masiku, mtsinjewo unaphwa chifukwa mvula sinagwe
m’dzikomo. 8 Yehova anayankhula naye kuti, 9 “Nyamuka tsopano,
pita ku Zarefati ku Sidoni ndipo ukakhale kumeneko. Ndalamula
mkazi wamasiye wa kumeneko kuti azikakudyetsa.” 10 Choncho iye
ananyamuka napita ku Zarefati. Atafika pa chipata cha mzindawo,
taonani mkazi wamasiye amatola nkhuni. Anamuyitana ndi kumuwuza
kuti, “Patseni madzi pang’ono m’chikho kuti ndimwe.” 11 Mayi wamasiye
uja ankapita kukatunga madzi, Eliya anamuyitananso namuwuza kuti,
“Chonde munditengerekonso buledi.”

12 Iye anayankha kuti “Pali Yehova Mulungu wanu wamoyo, ine ndilibe
chakudya china chilichonse, koma kaufa pang’ono m’mbiya ndi mafuta
pang’ono m’botolo. Ine ndikutola tinkhuni tochepa kuti ndipite nato ku
nyumba ndi kukaphika chakudya changa ndi cha mwana wanga, kuti
tikadye kenaka tife.”

13 Eliya anati kwa iye, “Musachite mantha. Pitani mukachite monga
mwaneneramo. Koma poyamba mundipangire kachakudya pang’ono
kuchokera pa ufa umene muli nawo ndi kubwera nako kwa ine, ndipo
kenaka mukaphike choti mudye inuyo ndi mwana wanuyo. 14 Pakuti
Yehova Mulungu wa Israeli akuti, ‘Ufa umene uli m’mbiyamo sudzatha
ndipo mafuta amene ali m’botolomo sadzathanso mpaka tsiku limene
Yehova adzagwetse mvula pa dziko lapansi.’ ”

15 Mayi wamasiyeyo anapita nakachita zimene Eliya anamuwuza.
Choncho panali chakudya cha Eliya, mayiyo pamodzi ndi banja lake lonse
chimene anadya masiku ambiri. 16 Pakuti ufa umene unali m’mbiya
sunathe ndiponso mafuta amene anali m’botolo sanathe, monga momwe
ananenera Yehova kudzera mwa Eliya.

17 Tsiku lina mwana wake wa mkazi wamasiye uja, mwini nyumbayo,
anadwala. Matenda ananka nakulirakulirabe, ndipo kenaka analeka
kupuma. 18 Mayiyo anati kwa Eliya, “Kodi ndakulakwirani chiyani, inu
munthu wa Mulungu? Kodi munabwera kuno kudzandikumbutsa tchimo
langa ndi kudzandiphera mwana wanga?”

19 Eliya anayankha kuti, “Patseni mwana wanuyo.” Iye anatenga
mwanayo m’manja mwa mayiyo napita naye m’chipinda chapamwamba,
kumene Eliyayo amagona, namugoneka pa bedi lake. 20 Kenaka Eliya
anafuwula kwa Yehova nati, “Inu Yehova Mulungu wanga, kodi mwab-
weretsanso choyipa chotere pa mkazi wamasiye amene ine ndikukhala

naye, pakuchichititsa kuti mwana wake afe?” 21 Pamenepo Eliya anakumbat-
ira mwanayo katatu ndi kufuwula kwa Yehova kuti, “Inu Yehova Mulungu
wanga, mubwezereni mwanayu moyo wake!”

22 Yehova anamva kufuwula kwa Eliya, ndipo moyo wa mwanayo
unabwerera mwa iye ndipo anatsitsimuka. 23 Eliya ananyamula mwanayo
natsika naye kuchoka m’chipinda chapamwamba chija nalowa naye
m’nyumba. Anamupereka kwa amayi ake ndipo anati, “Taonani, mwana
wanu ali ndi moyo!”

24 Pamenepo mayiyo anati kwa Eliya, “Tsopano ndadziwa kuti ndinu
munthu wa Mulungu ndipo mawu a Yehova amene mumayankhula ndi
owona.”

# 18

*Eliya ndi Obadiya*

1 Patapita masiku ambiri, m’chaka chachitatu cha chilala, Yehova
anayankhula ndi Eliya kuti, “Pita ukadzionetse kwa Ahabu ndipo ndidza-
gwetsa mvula pa dziko lapansi.” 2 Choncho Eliya anapita kukadzionetsa
kwa Ahabu.

Tsono nthawi imeneyi njala inakula kwambiri mu Samariya, 3 ndipo
Ahabu anayitana Obadiya amene ankayang’anira nyumba yake yaufumu.
(Obadiya ankaopa Yehova kwambiri. 4 Pamene Yezebeli ankapha aneneri
a Yehova, Obadiya anatenga aneneri 100 ndi kuwabisa m’mapanga awiri,
phanga lililonse aneneri makumi asanu, ndipo ankawapatsa chakudya ndi
madzi). 5 Ahabu anawuza Obadiya kuti, “Pita m’dziko kulikonse kumene
kuli zitsime za madzi ndi ku zigwa zonse. Mwina mwake tingapeze udzu
oti n’kumadyetsa akavalo ndi abulu kuti akhale ndi moyo, kuti tisaphe
chiweto chilichonse.” 6 Choncho anagawana dziko loti apiteko, Ahabu
anapita mbali ina, Obadiya n’kupita ina.

7 Obadiya akuyenda m’njira anakumana ndi Eliya. Ndipo taonani,
Obadiya anamuzindikira Eliyayo, naweramira pansi ndipo anati, “Kodi
ndinu, mbuye wanga Eliya?”

8 Eliya anayankha kuti, “Inde. Pita kawuze mbuye wako kuti, ‘Eliya
wabwera.’ ”

9 Obadiya anafunsa kuti, “Kodi ndalakwa chiyani kuti inu mupereke
mtumiki wanu kwa Ahabu kuti akaphedwe? 10 Pali Yehova Mulungu
wanu wamoyo, kulibe mtundu wa anthu kapena ufumu uliwonse kumene
mbuye wanga sanatumeko anthu okakufunafunani. Ndipo pamene
mtundu wa anthu kapena ufumu unena kuti kuno kulibe, Ahabu
ankawalumbiritsa kuti atsimikizedi kuti inuyo kulibe kumeneko. 11 Koma
tsopano mukundiwuza kuti ndipite kwa mbuye wanga ndi kukanena
kuti, ‘Eliya wabwera.’ 12 Ine sindikudziwa kumene Mzimu wa Yehova
udzakupititsani ine ndikachoka. Ngati ndipita kukamuwuza Ahabu ndipo
iye wosadzakupezani, adzandipha. Komatu ine mtumiki wanu ndakhala
ndi kupembedza Yehova kuyambira ubwana wanga. 13 Mbuye wanga,
kodi simunamve zimene ndinachita pamene Yezebeli ankapha aneneri a
Yehova? Ine ndinabisa aneneri 100 a Yehova m’mapanga awiri, m’phanga
lililonse aneneri makumi asanu, ndipo ndinkawapatsa chakudya ndi
madzi akumwa. 14 Ndiye inu tsopano mukundiwuza kuti ndipite kwa
mbuye wanga ndi kukanena kuti, ‘Eliya wabwera.’ Iyeyo adzandipha
ndithu!”

15 Eliya anati, "Pali Yehova Wamphamvuzonse wamoyo, amene ndima-
mutumikira, ine lero ndidzaonekera ndithu pamaso pa Ahabu."

### *Eliya pa Phiri la Karimeli*

16 Choncho Obadiya anapita kukakumana ndi Ahabu, namuwuza, ndipo
Ahabu anapita kukakumana ndi Eliya. 17 Pamene Ahabu anaona Eliya,
anati kwa iye, "Kodi ndiwedi, munthu wovutitsa Israeli uja?"
18 Eliya anayankha kuti, "Ine sindinavutitse Israeli, koma ndinuyo ndi
banja lanu. Mwasiya malamulo a Yehova ndipo mwatsatira Abaala.
19 Tsopano sonkhanitsani anthu a m'dziko lonse la Israeli kuti akumane
nane pa Phiri la Karimeli. Ndipo mubwere nawo aneneri a Baala 450 ndi
aneneri a fano la Asera 400, amene amadya pa tebulo la Yezebeli."
20 Choncho Ahabu anatumiza mawu m'dziko lonse la Israeli, ndipo
anasonkhanitsa aneneri a Baala ku Phiri la Karimeli. 21 Eliya anapita
patsogolo pa anthuwo ndipo anati, "Kodi mudzakhala anthu a mitima iwiri
mpaka liti? Ngati Yehova ndi Mulungu, mutsateni; koma ngati Baala ndi
Mulungu, mutsateni."

Koma anthu aja sanayankhe.

22 Pamenepo Eliya ananena kwa iwo kuti, "Ine ndilipo ndekha mneneri
wa Yehova, koma Baala ali ndi aneneri 450. 23 Tibweretsereni ng'ombe
zazimuna ziwiri. Iwo asankhepo okha ng'ombe imodzi, ndipo ayidule
nthulinthuli ndi kuziyika pa nkhuni nthulizo, koma osakolezapo moto.
Ndipo ine ndidzadula nthulinthuli ng'ombe inayo ndi kuyika pa nkhuni
koma sindikolezapo moto. 24 Kenaka inu muyitane dzina la mulungu
wanu, ndipo ine ndidzayitana dzina la Yehova. Mulungu amene ati
ayankhe potumiza moto, iyeyo ndiye Mulungu."

Pamenepo anthu onse anati, "Izi mwanena zamveka bwino."

25 Eliya anawuza aneneri a Baala kuti, "Yambani ndinu. Sankhani
ng'ombe yayimuna imodzi, muyikonze, popeza mulipo ambiri. Muyitane
dzina la mulungu wanu, koma musakoleze moto." 26 Choncho iwo
anatenga ng'ombe yayimunayo imene anawapatsa, nayikonza.

Kenaka anayitana dzina la Baala kuyambira mmawa mpaka masana.
Iwo anafuwula kuti, "Inu Baala, tiyankheni ife." Koma panalibe
yankho; palibe amene anayankha. Ndipo anavinavina mozungulira guwa
lansembe limene anapanga.

27 Nthawi yamasana Eliya anayamba kuwanyogodola ndipo anati,
"Fuwulani kwambiri. Ndithudi, iye ndi mulungu! Mwinatu akulingalira
kwambiri, kapena watanganidwa, kapena ali paulendo. Mwina wagona
ndipo n'kofunika kuti adzutsidwe." 28 Choncho iwo anafuwula kwambiri
ndi kudzichekacheka ndi malupanga ndi mikondo, potsata miyambo
yawo, mpaka kutuluka magazi. 29 Nthawi yamasana inadutsa, ndipo
anapitiriza kunenera mwakhama mpaka nthawi yopereka nsembe ya
madzulo. Koma panalibe yankho. Palibe amene anayankha, kapena
kulabadira zimenezo.

30 Pamenepo Eliya anati kwa anthu onse, "Senderani pafupi ndi ine."
Ndipo anthu onsewo anasendera pafupi ndi iye, ndipo iye anakonza guwa
lansembe la Yehova limene linali litawonongeka. 31 Eliya anatenga miyala
12, mwala uliwonse kuyimira fuko lililonse la Yakobo, amene Yehova
anamuwuza kuti, "Dzina lako lidzakhala Israeli." 32 Ndi miyala imeneyo
anamanga guwa m'dzina la Yehova, ndipo anakumba ngalande yayikulu
yolowa malita 15 a madzi kuzungulira guwalo. 33 Anayika nkhuni zija
m'malo mwake nadula nthulinthuli ng'ombe yayimuna ija ndi kuyika

nthulizo pa nkhunipo. Pamenepo Eliya anati, “Dzazani mitsuko inayi ndi madzi ndipo muwathire pa nyama ya nsembeyo ndi nkhunizo.”
34 Eliya anati, “Thiraninso kachiwiri.” Anthu aja anathiranso madziwo kachiwiri.
Iye analamula kuti, “Thiraninso kachitatu.” Ndipo iwo anathiranso
kachitatu. 35 Madziwo anayenderera pansi kuzungulira guwa lansembe, nadzaza ngalande yonse.
36 Pa nthawi yopereka nsembe, mneneri Eliya anasendera pafupi ndi guwa lansembe, napemphera kuti, “Inu Yehova, Mulungu wa Abrahamu, Isake ndi Yakobo, lero zidziwike kuti ndinu Mulungu mu Israeli ndipo kuti ine ndine mtumiki wanu, kuti ine ndachita zonsezi chifukwa mwalamula
ndinu. 37 Ndiyankheni, Inu Yehova, ndiyankheni, kuti anthu awa adziwe Inu Yehova, kuti ndinu Mulungu, ndipo kuti mutembenuziranso mitima yawo kwa Inu.”
38 Pamenepo moto wa Yehova unagwa, nunyeketsa nsembe yopserezayo, nkhuni, miyala ndi dothi lomwe. Unawumitsanso madzi amene anali m’ngalande.
39 Anthu onse ataona zimenezi, anaweramitsa nkhope zawo pansi, nafuwula kuti, “Yehova ndiye Mulungu! Yehova ndiye Mulungu!”
40 Pamenepo Eliya analamula anthuwo kuti, “Gwirani aneneri a Baala. Musalole kuti wina aliyense athawe!” Anagwira onsewo ndipo Eliya anabwera nawo ku Chigwa cha Kisoni, nawapha kumeneko.
41 Ndipo Eliya anati kwa Ahabu, “Pitani, kadyeni ndi kumwa, pakuti
kukumveka mkokomo wa mvula.” 42 Choncho Ahabu anapita kukadya ndi kumwa, koma Eliya anakwera pamwamba pa Phiri la Karimeli, ndipo anawerama mpaka pansi, nayika mutu wake pakati pa mawondo ake.
43 Eliya anawuza mtumiki wake kuti, “Pita kayang’ane ku nyanja.” Ndipo iye anapita nakayang’ana.
Mtumikiyo anati, “Kulibe kanthu.”
Kasanu n’kawiri Eliya anati, “Pitanso.”
44 Ulendo wachisanu ndi chiwiri mtumikiyo anafotokoza kuti, “Taonani, kamtambo kakang’ono kokhala ngati dzanja la munthu kakutuluka ku nyanja.”
Pamenepo Eliya anati, “Pita, kamuwuze Ahabu kuti, ‘Konzani galeta lanu ndipo mutsike mvula isanakutsekerezeni.’ ”
45 Nthawi imeneyi n’kuti kuthambo kutayamba kusonkhana mitambo yakuda, mphepo inawomba, mvula yamphamvu inagwa ndipo Ahabu
anakwera galeta napita ku Yezireeli. 46 Dzanja la Yehova linali pa Eliya ndipo atamangira lamba chovala chake, anathamanga ndi kumupitirira Ahabu mpaka kukhala woyamba kukafika ku Yezireeli.

# 19

### *Eliya Athawira ku Phiri la Horebu*

1 Tsono Ahabu anawuza Yezebeli zonse zimene anachita Eliya ndi
momwe anaphera aneneri onse ndi lupanga. 2 Choncho Yezebeli anatuma mthenga kwa Eliya kuti akamuwuze kuti, “Milungu indilange, ndipo indilange koopsa, ngati mawa nthawi ngati yomwe ino sindidzakupha iwe monga unaphera aneneriwo.”
3 Eliya ataona zimenezi, ananyamuka nathawa kupulumutsa moyo wake. Atafika ku Beeriseba ku Yuda, anasiya mtumiki wake kumeneko,
4 ndipo Eliyayo anayenda ulendo wa tsiku limodzi m’chipululu. Anafika

pa kamtengo ka tsache, nakhala pansi pa tsinde lake napemphera kuti
afe. Iye anati, “Yehova, ine ndatopa nazo. Chotsani moyo wanga. Ineyo
sindine wopambana makolo anga.” 5 Ndipo Eliya anagona tulo tofa nato
pa tsinde pa kamtengoko.

Ndipo taonani, mngelo anamukhudza, namuwuza kuti, “Dzuka udye.”
6 Eliya anayang’ana, ndipo taonani kumutu kwake kunali buledi wootcha
pa makala ndi botolo la madzi. Iye anadya ndi kumwa, n’kugonanso.

7 Mngelo wa Yehova anabweranso kachiwiri, anamukhudza, namuwuza
kuti, “Dzuka udye, popeza ulendowu ndi wautali.” 8 Tsono Eliya anadzuka
nadya ndi kumwa. Atapeza mphamvu chifukwa cha chakudyacho,
anayenda masiku 40, usana ndi usiku mpaka anafika ku Horebu, phiri
la Mulungu. 9 Kumeneko analowa m’phanga, nakhala komweko.

### *Ambuye Aonekera Eliya*

Ndipo taonani, Yehova anayankhula naye kuti, “Eliya, ukuchita chiyani
kuno?”

10 Iye anayankha kuti, “Ndakhala wodzipereka kwambiri kwa Yehova
Mulungu Wamphamvuzonse. Aisraeli asiya pangano lanu, agwetsa
maguwa anu ansembe, ndipo apha aneneri anu ndi lupanga. Ndatsala
ine ndekha ndipo tsopano akufuna kundipha.”

11 Yehova anati, “Tuluka ndipo ukayime pa phiri pamaso pa Yehova,
pakuti Yehova ali pafupi kudutsa pamenepo.”

Tsono mphepo yayikulu ndi yamphamvu inawomba ning’amba
mapiri ndi kuswa matanthwe pamaso pa Yehova, koma Yehova sanali
m’mphepomo. Itapita mphepoyo panachita chivomerezi, koma Yehova
sanali m’chivomerezicho. 12 Chitapita chivomerezicho, panafika moto,
koma Yehova sanali m’motomo. Ndipo utapita motowo, panamveka
kamphepo kayaziyazi. 13 Eliya atamva kamphepoko, anakokera chovala
chake naphimba kumutu. Anatuluka ndipo anayima pa khomo la phanga.

Ndipo panamveka mawu akuti, “Eliya, ukuchita chiyani kuno?”

14 Iye anayankha kuti, “Ndakhala wodzipereka kwambiri kwa Yehova
Mulungu Wamphamvuzonse. Aisraeli asiya pangano lanu, agwetsa
maguwa anu ansembe, ndipo apha aneneri anu ndi lupanga. Ndatsala
ine ndekha ndipo tsopano akufuna kundipha.”

15 Yehova anati kwa Eliyayo, “Bwerera njira imene unadzera, ndipo
upite ku Chipululu cha ku Damasiko. Ukakafika kumeneko, ukadzoze
Hazaeli kuti akhale mfumu ya ku Aramu. 16 Ukadzozenso Yehu mwana
wa Nimisi kuti akhale mfumu ya Israeli, ndiponso ukadzoze Elisa mwana
wa Safati wa ku Abeli-Mehola kuti akhale mneneri wolowa m’malo
mwako. 17 Yehu adzapha aliyense amene adzapulumuke ku lupanga la
Hazaeli, ndipo Elisa adzapha aliyense amene adzapulumuke ku lupanga
la Yehu. 18 Komabe ndasunga anthu 7,000 ku Israeli, anthu onse
amene mawondo awo sanagwadirepo Baala, onse amene pakamwa pawo
sipanapsompsoneko fano lake.”

### *Kuyitanidwa kwa Elisa*

19 Kotero Eliya anachoka kumeneko, nakapeza Elisa mwana wa Safati.
Iye ankatipula ndi mapulawo khumi ndi awiri okokedwa ndi ng’ombe
ziwiriziwiri zapamagoli, ndipo iye mwini ankayendetsa goli la khumi
ndi chiwiri. Eliya anapita kumene anali namuveka chofunda chake.
20 Pomwepo Elisa anasiya ng’ombe zake nathamangira Eliya. Iye anati,

“Mundilole kuti ndikatsanzike abambo ndi amayi anga, ndipo kenaka
ndidzakutsatani.”
Eliya anayankha kuti, “Bwerera. Ine ndachita chiyani kwa iwe?”
21 Choncho Elisa anamusiya Eliyayo nabwerera kwawo. Anatenga
ng’ombe zake ziwiri zapagoli nazipha. Anatenga magoli a mapulawo ake
nasonkhera moto kuphikira nyamayo ndipo anayipereka kwa anthu kuti
adye. Ndipo ananyamuka natsatira Eliya ndi kukhala mtumiki wake.

# 20

*Beni-Hadadi Athira Nkhondo Samariya*

1 Tsono Beni-Hadadi mfumu ya ku Aramu inasonkhanitsa magulu ake
onse a ankhondo. Iye pamodzi ndi mafumu 32, akavalo awo ndi magaleta
awo, anapita kukawuzungulira mzinda wa Samariya ndi kuwuthira
nkhondo. 2 Iye anatuma amithenga ake mu mzindamo kwa Ahabu mfumu
ya Israeli, kukanena kuti, 3 “Beni-Hadadi akuti, ‘Siliva wako ndi golide
wako ndi wanga, ndipo akazi ako okongola ndi ana ako ndi anganso.’ ”
4 Mfumu ya Israeli inayankha kuti, “Monga mmene mwanenera, mbuye
wanga mfumu, ine pamodzi ndi zonse zomwe ndili nazo ndi zanu.”
5 Amithenga aja anabwereranso kwa Ahabu ndipo anamuwuza kuti,
“Beni-Hadadi akuti, ‘Ine ndinakulamula kuti undipatse siliva wako ndi
golide wako, akazi ako ndi ana ako. 6 Koma mawa nthawi ngati yomwe
ino ndidzatuma atumiki anga kudzafufuza m’nyumba yako yaufumu
ndi nyumba za akuluakulu ako. Iwo adzatenga chilichonse chimene
umachidalira ndi kupita nacho.’ ”
7 Pamenepo mfumu ya Israeli inayitanitsa akuluakulu a m’dzikomo
niwawuza kuti, “Taonani momwe munthuyu akufunira kutibweretsera
mavuto! Atatumiza mawu oti ndimupatse akazi anga ndi ana anga, siliva
wanga ndi golide wanga, ine sindinamukanize.”
8 Akuluakulu onse ndi anthu onse anayankha kuti, “Musamumvere
kapena kuvomereza zofuna zake.”
9 Tsono Ahabu anayankha amithenga a Beni-Hadadi kuti, “Kamuwuzeni
mbuye wanga mfumu kuti, ‘Mtumiki wanu adzachita zonse zimene
munazifuna nthawi yoyamba ija, koma izi mwazifunazi sindingazikwan-
itse.’ ” Iwo anachoka nakapereka yankho kwa Beni-Hadadi.
10 Pamenepo Beni-Hadadi anatumizanso uthenga wina kwa Ahabu kuti,
“Milungu indilange koopsa, ngati mu Samariya mudzakhale fumbi loti
n’kudzaza dzanja la aliyense wa anthu anga.”
11 Mfumu ya Israeli inayankha kuti, “Kamuwuzeni kuti, ‘Mwamuna
mnzako n’pachulu, n’kulinga utakwerapo.’ ”
12 Beni-Hadadi anamva uthenga umenewu pamene iye ankamwa
ndi mafumu anzake m’matenti awo, ndipo analamula anthu ake kuti,
“Konzekerani kukathira nkhondo.” Choncho anakonzekera kukathira
nkhondo mzindawo.

*Ahabu Agonjetsa Beni-Hadadi*

13 Ndipo taonani, mneneri wina anabwera kwa Ahabu mfumu ya Israeli
nadzalengeza kuti, “Yehova akuti, ‘Kodi ukuchiona chigulu chachikulu
cha ankhondochi? Taona, ndikuchipereka chimenechi lero m’dzanja lako,
ndipo pamenepo udzadziwa kuti Ine ndine Yehova.’ ”
14 Ahabu anafunsa kuti, “Koma ndani adzachita zimenezi?”

Mneneri anayankha kuti, “Yehova akuti, ‘Adzachita zimenezi ndi asilikali a nduna za m’zigawo.’ ”

Ndipo iye anafunsa kuti, “Kodi ndani adzayambe nkhondoyi?”

Mneneriyo anayankha kuti, “Ndinu.”

15 Choncho Ahabu anawerenga asilikali achinyamata a nduna za
m’zigawo ndipo onse analipo 232. Ndipo anawerenganso ankhondo a ku
Israeli ndipo onse analipo 7,000. 16 Iwo ananyamuka nthawi yamasana
pamene Beni-Hadadi ndi mafumu 32 othandizana naye ankamwa mpaka
kuledzera m’matenti awo. 17 Asilikali achinyamata a nduna za m’zigawo
ndiwo amene anayamba kupita ku nkhondo.

Nthawi imeneyi Beni-Hadadi n’kuti atatumiza anthu oti akazonde, amene anadzafotokoza kuti, “Anthu ankhondo akubwera kuchokera ku Samariya.”

18 Iye anati, “Kaya akubwera mwamtendere kapena mwankhondo, muwagwire amoyo.”

19 Choncho asilikali achinyamata a nduna za m’zigawo anatuluka mu
mzinda, gulu lankhondo lili pambuyo pawo. 20 Ndipo aliyense wa iwo
anapha munthu wake. Ataona izi, Aaramu anathawa Aisraeli ali pambuyo
pawo kuwapirikitsa. Koma Beni-Hadadi mfumu ya ku Aaramu anathawa
atakwera pa kavalo pamodzi ndi ankhondo ena okweranso pa akavalo.
21 Mfumu ya Israeli inapita chitsogolo ndi kugwira akavalo ndi magaleta
ndipo Aaramu ambiri anaphedwa.

22 Zitachitika izi, mneneri wina anabwera kwa mfumu ya Israeli ndipo anati, “Mulimbike ndipo muganize bwino zoti mudzachite, chifukwa chaka chikudzachi mfumu ya Aramu idzakuthiraninso nkhondo.”

23 Nthawi imeneyi, akuluakulu a mfumu ya Aramu anamulangiza kuti,
“Milungu ya anthu a ku Israeli ndi milungu ya m’mapiri. N’chifukwa
chake anali ndi mphamvu zotipambana ife. Koma ngati tidzamenyana
nawo ku chigwa, ndithudi ife tidzakhala ndi mphamvu kuposa iwo. 24 Inu
chitani izi: chotsani mafumu onse pa maudindo awo ndipo m’malo
mwawo muyikemo atsogoleri a ankhondo. 25 Musonkhanitsenso gulu
lankhondo lofanana ndi lomwe linaphedwa lija, akavalo monga omwe
anaphedwa aja, ndi magaleta monga omwe anawonongedwa aja, kuti
tikamenyane ndi Israeli ku chigwa. Pamenepo, ife tidzapambana iwowo.”
Beni-Hadadi anagwirizana nawo ndipo anachita momwemo.

26 Chaka chinacho Beni-Hadadi anasonkhanitsa Aaramu, napita ku
Afeki kukamenyana ndi Israeli. 27 Aisraeli atasonkhananso, napatsidwa
zakudya zawo anapita kukakumana nawo. Aisraeli anamanga misasa
yawo moyang’anana ndi Aaramu ndipo ankaoneka ngati timagulu tiwiri
ta mbuzi, pomwe Aaramu anali atakuta dera lonselo.

28 Munthu wa Mulungu anabwera, nawuza mfumu ya Israeli kuti, “Yehova akuti, ‘Popeza Aaramu akuganiza kuti Yehova ndi mulungu wa ku mapiri, osati wa ku zigwa, Ine ndidzapereka chigulu chonsechi kwa iwe, ndipo iwe udzadziwa kuti Ine ndine Yehova.’ ”

29 Kwa masiku asanu ndi awiri anakhala moyang’anana m’misasa yawo,
ndipo pa tsiku lachisanu ndi chiwiri nkhondo inayambika. Aisraeli
anapha Aaramu okwana 100,000 tsiku limodzi lokha. 30 Ena onse otsala
anathawira ku Afeki, kumene khoma linagwera anthu 27,000. Ndipo Beni-
Hadadi anathawira mu mzinda, nakabisala m’chipinda cham’kati.

31 Atumiki ake anamuwuza kuti, “Taonani, ife tamva kuti mafumu a fuko
la Israeli ndi achifundo. Tiyeni tipite kwa mfumu ya ku Israeli titavala

ziguduli m'chiwuno mwathu ndi kumanga zingwe m'makosi mwathu.
Mwina iye sakakuphani."
32 Atavala ziguduli m'chiwuno mwawo ndi kumanga zingwe m'makosi
mwawo, anapita kwa mfumu ya ku Israeli ndipo anayiwuza kuti,
"Mtumiki wanu Beni-Hadadi akunena kuti, 'Chonde loleni kuti ndikhale
moyo.' "
Mfumu inayankha kuti, "Kodi iye akanali ndi moyo? Iye ujatu ndi
m'bale wanga."
33 Anthuwo ankaganiza kuti mawuwo anali abwino ndipo anavomereza
mawuwa mofulumira. Iwo anati, "Inde, Beni-Hadadi ndi m'bale wanu!"
Mfumu inati, "Pitani kamutengeni." Beni-Hadadi atatuluka, Ahabu
anamukweza m'galeta lake.
34 Beni-Hadadi anawuza Ahabu kuti, "Ndidzabweza mizinda imene
abambo anga analanda abambo anu. Ndipo mutha kumanga nyumba
zanu zamalonda mu Damasiko, monga anachitira abambo anga ku
Samariya."
Ahabu anati, "Chifukwa cha mgwirizano umenewu, ine ndidzakuma-
sula." Choncho anachita naye mgwirizano, ndipo anamulola kuti apite.

### *Mneneri Adzudzula Ahabu*

35 Molamulidwa ndi Yehova, mmodzi mwa ana a aneneri anawuza
mnzake kuti, "Chonde, menye ndi chida chako," koma mnzakeyo anakana.
36 Choncho mneneriyo anati, "Chifukwa sunamvere Yehova, ukango-
choka pano, mkango ukupha." Ndipo munthuyo atangochoka pamenepo,
mkango unamupeza ndi kumupha.
37 Mneneriyo anapeza munthu wina ndipo anamuwuza kuti, "Chonde,
menye." Choncho munthuyo anamumenya ndi kumuvulaza. 38 Pamenepo
mneneriyo anapita nakayima pa msewu kudikirira mfumu. Iye anadzibisa
nakulunga nsalu nkhope yake. 39 Mmene mfumu inkadutsa pamenepo,
mneneriyo anafuwula kwa mfumuyo kuti, "Ine mtumiki wanu ndinalowa
pakati pa nkhondo, ndipo munthu wina anabwera kwa ine atatenga
mmodzi mwa anthu ogwidwa pa nkhondo, nandiwuza kuti, 'Sunga
munthu uyu. Ngati asowa, ndiye kuti ndidzakupha, kapena udzalipira
ndalama 3,000 za siliva.' 40 Pamene ine mtumiki wanu ndinali wotan-
ganidwa apa ndi apa, munthuyo anasowa."
Mfumu ya Israeli inati, "Chimenechi ndiye chilango chako. Iwe
wadziweruza wekha."
41 Pamenepo mneneriyo anachotsa msangamsanga nsalu yomwe anaku-
lunga pa nkhope yake, ndipo mfumu ya Israeli inamuzindikira kuti ndi
mmodzi mwa aneneri. 42 Iye anawuza mfumu kuti, "Yehova akuti,
'Chifukwa chakuti mwamasula munthu amene Ine ndinati ndi woyenera
kuphedwa, inuyo ndi amene mudzaphedwe m'malo mwa iyeyo, anthu anu
m'malo mwa anthu ake.' " 43 Mwachisoni ndi mokwiya, mfumu ya Israeli
inapita ku nyumba yake yaufumu ku Samariya.

## 21

### *Munda Wamphesa wa Naboti*

1 Zitatha izi, panachitika nkhani yokhudza Naboti wa ku Yezireeli amene
anali ndi munda wamphesa ku Yezireeli, pafupi ndi nyumba ya mfumu
Ahabu, mfumu ya ku Samariya. 2 Ahabu anawuza Naboti kuti, "Patse
munda wako wa mpesa kuti ukhale munda wanga wa ndiwo zamasamba,

popeza uli pafupi ndi nyumba yanga yaufumu. Mosinthana ndi mundawu
ndidzakupatsa wina wabwino, kapena ngati ungafune, ndidzakupatsa
ndalama pa mtengo wake wa mundawu."

3 Koma Naboti anayankha Ahabu kuti, "Pali Yehova, sindingakupatseni
cholowa cha makolo anga."

4 Pamenepo Ahabu anapita ku nyumba yake, wachisoni ndi wokwiya
chifukwa Naboti wa ku Yezireeli anamuwuza kuti, "Sindidzakupatsani
cholowa cha makolo anga." Ahabu anakagona pa bedi lake atayang'ana
kumbali ndipo anakana chakudya.

5 Yezebeli mkazi wake analowa ndipo anamufunsa kuti, "Chifukwa
chiyani mukuoneka achisoni? Chifukwa chiyani simukufuna chakudya?"

6 Ahabu anayankha mkazi wake kuti, "Chifukwa chake n'chakuti ine
ndinamuwuza Naboti wa ku Yezireeli kuti, 'Gulitse munda wako wa mpesa
kapena ngati ungakonde ine ndidzakupatsa munda wina wabwino m'malo
mwake.' Koma iye anandiyankha kuti, 'Sindidzakupatsani munda wanga
wa mpesa.' "

7 Ndipo Yezebeli mkazi wake anati, "Kodi umu ndi mmene mumachitira
ngati mfumu ya Israeli? Dzukani, idyani! Sangalalani. Ine ndidza-
kutengerani munda wamphesa wa Naboti wa ku Yezireeli."

8 Choncho Yezebeli analemba makalata m'dzina la Ahabu, nawadinda
chidindo cha mfumu, nawatumiza makalatawo kwa akuluakulu ndi kwa
anthu olemekezeka amene ankakhala ndi Naboti mu mzinda mwake.
9 M'makalatamo Yezebeli analemba kuti:

> "Lengezani kuti anthu asale chakudya ndipo muyike Naboti pa malo
> aulemu pakati pa anthu. 10 Koma muyike anthu awiri oyipa mtima
> moyang'anana naye ndipo iwo achitire umboni kuti watemberera
> Mulungu ndiponso mfumu. Ndipo mumutulutse ndi kumuponya miyala
> ndi kumupha."

11 Choncho akuluakulu ndi anthu olemekezeka amene ankakhala
ndi Naboti mu mzinda mwake anachita monga analamulira Yezebeli
m'makalata amene anawalembera. 12 Iwo analengeza kuti anthu asale
chakudya ndipo anayika Naboti pa malo aulemu pakati pa anthu.
13 Ndipo anthu awiri oyipa anabwera nakhala moyang'anana naye ndipo
anamunenera zoyipa Naboti pamaso pa anthu, ponena kuti, "Naboti
watemberera Mulungu ndiponso mfumu." Choncho anamutulutsira kunja
kwa mzinda ndi kumuponya miyala ndi kumupha. 14 Atatero anatumiza
mawu kwa Yezebeli akuti, "Naboti amuponya miyala ndipo wafa."

15 Yezebeli atangomva kuti Naboti amuponya miyala ndipo wafa, iye
anakamuwuza Ahabu kuti, "Dzukani, katengeni munda wamphesa wa
Naboti wa ku Yezireeli umene anawukaniza kukugulitsani. Naboti sali
moyonso, koma wafa." 16 Ahabu atamva kuti Naboti wafa, ananyamuka
kukatenga munda wamphesa wa Naboti.

17 Ndipo Yehova anayankhula ndi Eliya wa ku Tisibe kuti, 18 "Nyamuka,
pita ukakumane ndi Ahabu, mfumu ya Israeli amene amalamulira ku
Samariya. Pano ali ku munda wamphesa wa Naboti kumene wapita
kuti akatenge mundawo kuti ukhale wake. 19 Ukamuwuze kuti: 'Yehova
akuti, Kodi siwapha munthu ndi kumulandanso munda wake?' Ndipo
ukamuwuzenso kuti, 'Yehova akuti, Pamalo pamene agalu ananyambita
magazi a Naboti, pamalo pomwepo agalu adzanyambita magazi ako, inde,
akonso!' "

20 Ahabu anati kwa Eliya, "Tsono wandipeza, iwe mdani wanga!"

Eliya anayankha kuti, “Inde ndakupezani chifukwa mwadzigulitsa kuti
muchite zoyipa pamaso pa Yehova. 21 Iye akuti ‘Taonani, ine ndidzab-
weretsa mavuto pa iwe. Ndidzawononga kotheratu zidzukulu zako ndi
kuchotsa mu Israeli munthu aliyense wamwamuna wa banja la Ahabu,
kapolo kapena mfulu. 22 Ndidzawononga nyumba yako monga momwe
ndinawononongera nyumba ya Yeroboamu mwana wa Nebati ndiponso
ngati nyumba ya Baasa mwana wa Ahiya, chifukwa wandikwiyitsa Ine
ndi kuchimwitsa Israeli.’

23 “Ndipo kunena za Yezebeli, Yehova akuti, ‘Agalu adzadya Yezebeli
m’mbali mwa khoma la Yezireeli.’

24 “Agalu adzadya munthu aliyense wa nyumba ya Ahabu amene
adzafere mu mzinda, ndipo mbalame za mu mlengalenga zidzadya
aliyense wofera ku thengo.”

25 (Kunalibe munthu ngati Ahabu, amene anadzigulitsa kuchita zoyipa
pamaso pa Yehova, amene anakopedwa ndi mkazi wake Yezebeli. 26 Iye
anachita zonyansa kwambiri popembedza mafano, monga mmene anka-
chitira Aamori amene Yehova anawachotsa pamene Aisraeli ankafika).

27 Ahabu atamva mawu amenewa, anang’amba zovala zake, navala
ziguduli ndi kusala chakudya. Anagona pa ziguduli, nayenda
pang’onopang’ono.

28 Pamenepo Yehova anayankhula ndi Eliya wa ku Tisibe kuti, 29 “Kodi
waona mmene Ahabu wadzichepetsera pamaso panga? Chifukwa
wadzichepetsa, sindidzabweretsa mavuto amenewa pa nthawi ya moyo
wake, koma ndidzawabweretsa pa nyumba yake pa nthawi ya mwana
wake.”

# 22

*Mikaya Anenera Motsutsa Ahabu*

1 Kwa zaka zitatu panalibe nkhondo pakati pa Aramu ndi Israeli. 2 Koma
pa chaka chachitatu, Yehosafati mfumu ya ku Yuda anapita kukacheza ndi
mfumu ya ku Israeli. 3 Mfumu ya ku Israeli n’kuti itawuza atumiki ake
kuti, “Kodi inu simukudziwa kuti Ramoti Giliyadi ndi dera lathu ndipo ife
palibe chimene tikuchita kuti tilitenge deralo m’manja mwa mfumu ya
Aramu?”

4 Tsono iye anafunsa Yehosafati kuti, “Kodi udzapita nane ku nkhondo
ku Ramoti Giliyadi?”

Yehosafati anayankha mfumu ya ku Israeli kuti, “Ine ndili monga inu,
anthu anga monga anthu anu, akavalo anga monga akavalo anu.” 5 Koma
Yehosafati anawuzanso mfumu ya ku Israeli kuti, “Poyamba mupemphe
nzeru kwa Yehova.”

6 Choncho mfumu ya Israeli inasonkhanitsa pamodzi aneneri okwanira
400, ndipo inawafunsa kuti, “Kodi ndipite kukathira nkhondo Ramoti
Giliyadi, kapena ndileke?”

Iwo anayankha kuti, “Pitani, pakuti Ambuye waupereka mzindawo
m’manja mwa mfumu.”

7 Koma Yehosafati anafunsa kuti, “Kodi kuno kulibenso mneneri wina
wa Yehova kumene ife tingakafunsireko nzeru?”

8 Mfumu ya ku Israeli inayankha Yehosafati kuti, “Alipo munthu mmodzi
amene ife tingakafunsire kwa Yehova, koma ndimadana naye chifukwa
iyeyo samanenera kanthu kalikonse kabwino ka ine, koma zoyipa nthawi
zonse. Dzina lake ndi Mikaya mwana wa Imula.”

Yehosafati anayankha kuti, “Mfumu musatero.”
9 Choncho mfumu ya Israeli inayitana mmodzi mwa atumiki ake ndipo
inati, “Kayitane Mikaya mwana wa Imula msangamsanga.”
10 Atavala mikanjo yawo yaufumu, mfumu ya ku Israeli ndi Yehosafati
mfumu ya ku Yuda anakhala pa mipando yawo yaufumu pabwalo lopon-
dera tirigu pafupi ndi chipata cha Samariya, pamodzi ndi aneneri onse
akunenera pamaso pawo. 11 Tsono Zedekiya mwana wa Kenaana n’kuti
atapanga nyanga zachitsulo ndipo iye ananenera kuti, “Yehova akuti, ‘Ndi
nyanga izi, inu mudzagunda nazo Aaramu mpaka iwo atawonongeka.’ ”
12 Aneneri ena onse ananenera zomwezonso. Iwo anati, “Kathireni
nkhondo Ramoti Giliyadi ndipo mukapambana, pakuti Yehova adzawu-
pereka mzindawo m’dzanja la mfumu.”
13 Wamthenga amene anapita kukayitana Mikaya anamuwuza kuti,
“Taonani, aneneri onse monga munthu mmodzi akunenera za kupambana
kwa mfumu. Mawu anunso akhale ogwirizana ndi mawu awo, ndipo
mukayankhule zabwino.”
14 Koma Mikaya anati, “Pali Yehova wamoyo, ine ndikawawuza zokhazo
zimene Yehova akandiwuze.”
15 Atafika, Ahabu anamufunsa kuti, “Mikaya, kodi tipite kukathira
nkhondo Ramoti Giliyadi, kapena tileke?”
Iye anayankha kuti, “Pitani ndipo mukapambana, pakuti Yehova
adzawupereka mzindawo m’dzanja la mfumu.”
16 Ahabu anati kwa iye, “Kodi ndikulumbiritse kangati kuti undiwuze
zoona zokhazokha m’dzina la Yehova?”
17 Pamenepo Mikaya anayankha kuti, “Ndinaona Aisraeli onse
atamwazikana pa mapiri ngati nkhosa zopanda m’busa, ndipo Yehova
anati, ‘Anthu awa alibe mbuye wawo. Aliyense apite kwawo mwamten-
dere.’ ”
18 Mfumu ya ku Israeli inati kwa Yehosafati, “Kodi ine sindinakuwuzeni
kuti ameneyu samanenera kanthu kalikonse kabwino ka ine, koma zoyipa
zokhazokha?”
19 Mikaya anapitiriza kuyankhula nati, “Tsono imvani mawu a Yehova:
Ine ndinaona Yehova atakhala pa mpando wake waufumu, gulu lonse la
kumwamba litayima ku dzanja lake lamanja ndi ku dzanja lake lamanzere.
20 Ndipo Yehova anati, ‘Kodi ndani amene akamukope Ahabu kuti akathire
nkhondo Ramoti Giliyadi, n’kukafera komweko?’ ”
“Wina anapereka maganizo ena ndipo winanso maganizo ena.
21 Potsirizira, mzimu wina unabwera ndi kuyima pamaso pa Yehova ndipo
unati, ‘Ine ndidzamukopa.’ ”
22 Yehova anafunsa kuti, “Ukamukopa bwanji?”
Mzimuwo unati, “Ndidzapita ndi kukakhala mzimu wabodza pakamwa
pa aneneri ake onse.”
Yehova anati, “ ‘Iwe udzamukopadi. Pita kachite zomwezo.’
23 “Ndipo tsopano taonani, Yehova wayika mzimu wabodza m’kamwa
mwa aneneri anu onsewa. Yehova waneneratu kuti mukaona mavuto.”
24 Pamenepo Zedekiya mwana wa Kenaana anapita pafupi namenya
Mikaya patsaya. Iye anafunsa Mikaya kuti, “Kodi mzimu wa Yehova
unadzera njira iti pamene umatuluka mwa ine kuti uziyankhula ndi iwe?”
25 Mikaya anayankha kuti, “Udzaona pa tsiku limene uzikalowa
m’chipinda cham’kati kuti ukabisale.”
26 Pamenepo mfumu ya ku Israeli inalamula kuti, “Mugwireni Mikaya
ndipo mubwerere naye kwa Amoni mkulu wa mzinda, ndi kwa Yowasi

mwana wa mfumu [27] ndipo mukanene kuti, ‘Chimene mfumu ikunena ndi ichi; Muyikeni m’ndende munthu uyu ndipo musamupatse chakudya china koma buledi ndi madzi pang’ono mpaka nditabwerera mwamtendere.’ ”
[28] Mikaya ananena kuti, “Ngati mudzabwerera mwamtendere, Yehova sanayankhule kudzera mwa ine.” Ndipo iye anapitiriza kunena kuti, “Gwiritsitsani mawu angawa, anthu inu nonse!”

### *Ahabu Aphedwa ku Ramoti Giliyadi*

[29] Choncho mfumu ya ku Israeli ndi Yehosafati mfumu ya ku Yuda
anapita ku Ramoti Giliyadi. [30] Mfumu ya ku Israeli inawuza Yehosafati kuti, “Ine ndidzalowa mu nkhondoyi modzibisa, koma inu muvale zovala zanu zaufumu.” Choncho mfumu ya ku Israeli inadzibisa ndi kupita ku nkhondo.
[31] Tsono mfumu ya ku Aramu n’kuti italamulira anthu ake 32 olamulira magaleta kuti, “Musamenyane ndi wina aliyense, wamng’ono kapena wamkulu, koma mfumu ya ku Israeli.” [32] Olamulira magaleta ataona Yehosafati, ankaganiza kuti, “Ndithu iyi ndiye mfumu ya ku Israeli.” Choncho anabwerera kukamenyana naye, koma Yehosafati atafuwula,
[33] olamulira akavalo anaona kuti sanali mfumu ya ku Israeli ndipo analeka kumuthamangitsa.
[34] Koma munthu wina anaponya muvi wake mwachiponyeponye ndi kulasa mfumu ya ku Israeli polumikizira malaya ake odzitetezera. Mfumu inawuza woyendetsa galeta lake kuti, “Tembenuka ndipo undichotse pa
nkhondo pano pakuti ndalasidwa.” [35] Nkhondo inakula kwambiri tsiku limenelo, ndipo mfumu inakhala tsonga m’galeta lake moyang’anana ndi Aaramu. Magazi ake ankayenderera pansi kuchokera m’galeta, ndipo pa
nthawi ya madzulo inamwalira. [36] Pamene dzuwa linkalowa, kunamveka mfuwu wa nkhondo kuti, “Munthu aliyense apite ku mzinda wa kwawo, aliyense apite ku dziko la kwawo!”
[37] Ndipo mfumu ija inafa, nabwera nayo ku Samariya, ndipo anayika
m’manda kumeneko. [38] Anatsuka galeta lija pa dziwe la ku Samariya (pamene ankasamba akazi achiwerewere) ndipo agalu ananyambita magazi a mfumuyo, monga momwe Yehova ananenera.
[39] Tsono ntchito zina za Ahabu, kuphatikiza zonse anazichita, nyumba yaufumu imene anamanga yokutidwa ndi minyanga ya njovu, mizinda yotetezedwa, kodi sizinalembedwe m’buku la mbiri ya mafumu a ku
Israeli? [40] Ahabu anamwalira nayikidwa m’manda pamodzi ndi makolo ake. Ndipo Ahaziya mwana wake analowa ufumu m’malo mwake.

### *Yehosafati Mfumu ya ku Yuda*

[41] Yehosafati, mwana wa Asa anakhala mfumu ya ku Yuda chaka
chachinayi cha Ahabu mfumu ya ku Israeli. [42] Yehosafati anali wa zaka 35 pamene analowa ufumu, ndipo analamulira ku Yerusalemu zaka 25.
Amayi ake anali Azuba mwana wa Silihi. [43] Pa zinthu zonse, Yehosafati anayenda m’njira za Asa abambo ake ndipo sanachite zotsutsana ndi machitidwe a abambo ake. Iye anachita zolungama pamaso pa Yehova. Komabe, malo azipembedzo sanawawononge, ndipo anthu anapitiriza
kupereka nsembe ndi kufukiza lubani kumeneko. [44] Yehosafati anakhala mwamtendere ndi mfumu ya ku Israeli.
[45] Ntchito zake zina za Yehosafati, zinthu zimene anachita ndi zamphamvu zimene anaonetsa, kodi sizinalembedwe m’buku la mbiri ya

mafumu a ku Yuda? 46 Iye anachotsa m'dzikomo amuna onse ochita zachi-
werewere mwa chipembedzo amene anatsalira pa nthawi ya ulamuliro wa
Asa, abambo ake. 47 Nthawi imeneyo kunalibe mfumu ku Edomu, amene
ankalamulira anali munthu woyikidwa ndi mfumu ya ku Yuda.

48 Yehosafati anapanga sitima zapamadzi zopita ku Ofiri kukatenga
golide, koma sitimazo sizinayende chifukwa zinawonongeka ku Ezioni
Geberi. 49 Nthawi imeneyo Ahaziya mwana wa Ahabu anawuza Yehosafati
kuti, "Anthu anga ayende pa madzi pamodzi ndi anthu anu," koma
Yehosafati anakana.

50 Ndipo Yehosafati anamwalira nayikidwa m'manda pamodzi ndi
makolo ake mu mzinda wa Davide. Ndipo Yoramu mwana wake analowa
ufumu m'malo mwake.

*Ahaziya Mfumu ya ku Israeli*

51 Ahaziya mwana wa Ahabu anakhala mfumu ya ku Israeli ku
Samariya m'chaka cha 17 cha Yehosafati mfumu ya ku Yuda, ndipo
analamulira Israeli zaka ziwiri. 52 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova,
chifukwa anayenda m'njira za abambo ndi amayi ake komanso m'njira za
Yeroboamu mwana wa Nebati, amene anachimwitsa Israeli. 53 Potumikira
ndi kupembedza Baala, iye anakwiyitsa Yehova Mulungu wa Israeli,
monga momwe anachitira abambo ake.

# 2 Mafumu

*Yehova Alanga Ahaziya*

1 Atamwalira Ahabu, Mowabu anawukira Israeli. 2 Ndipo Ahaziya
anagwa kuchokera pa khonde la chipinda chake chammwamba ku
Samariya, ndipo anavulala kwambiri. Choncho iye anatuma amithenga
nawawuza kuti, “Pitani mukafunse kwa Baala-zebubu, mulungu wa ku
Ekroni, ngati ndichire matendawa.”

3 Koma mngelo wa Yehova anawuza Eliya wa ku Tisibe kuti, “Nyamuka,
pita ukakumane ndi amithenga a mfumu ya ku Samariya ndipo ukawa-
funse kuti, ‘Kodi popeza kulibe Mulungu ku Israeli, n’chifukwa chake inu
mukupita kukafunsa nzeru kwa Baala-zebubu, mulungu wa ku Ekroni?’
4 Tsono Yehova akuti, ‘Iweyo sudzadzuka pa bedi wagonapo. Udzafa
ndithu!’ ” Ndipo Eliya ananyamuka.

5 Amithenga aja atabwerera kwa mfumu, mfumuyo inawafunsa kuti,
“Chifukwa chiyani mwabwerera?”

6 Iwo anayankha kuti, “Munthu wina anabwera kudzakumana nafe,
ndipo anatiwuza kuti, bwererani kwa mfumu imene inakutumani ndipo
mukayiwuze kuti, ‘Yehova akuti, kodi popeza kulibe Mulungu ku Israeli,
n’chifukwa chake mukupita kukafunsa nzeru kwa Baala-zebubu, mulungu
wa ku Ekroni? Tsono sudzadzuka pa bedi wagonapo. Udzafa ndithu!’ ”

7 Mfumu inafunsa amithengawo kuti, “Kodi munthu amene anabwera
kudzakumana nanuyo ndi kukuwuzani zimenezi amaoneka bwanji?”

8 Iwo anayankha kuti, “Munthuyo anavala zovala zaubweya ndi lamba
wachikopa m’chiwuno mwake.”

Mfumu inati, “Munthu ameneyo ndi Eliya wa ku Tisibe.”

9 Pamenepo mfumu inatuma mtsogoleri wa ankhondo ndi anthu ake
makumi asanu kwa Eliya. Mtsogoleriyo anapita kwa Eliya, amene anali
atakhala pamwamba pa phiri, ndipo anati, “Munthu wa Mulungu, mfumu
ikuti, ‘Tsikani!’ ”

10 Eliya anayankha mtsogoleriyo kuti, “Ngati ndine munthu wa Mu-
lungu, moto utsike kuchokera kumwamba, ukupsereze iwe pamodzi ndi
anthu makumi asanu akowo!” Pomwepo moto unatsikadi kuchokera
kumwamba ndipo unapsereza mtsogoleriyo pamodzi ndi anthu akewo.

11 Zitachitika izi, mfumu inatumanso mtsogoleri wina pamodzi ndi
asilikali ake makumi asanu. Mtsogoleriyo anati kwa Eliya, “Munthu wa
Mulungu, zimene mfumu ikunena ndi izi, ‘Tsikani msangamsanga!’ ”

12 Eliya anayankha kuti, “Ngati ndine munthu wa Mulungu, moto
utsike kuchokera kumwamba, ukupsereze iwe pamodzi ndi anthu ako
makumi asanuwo!” Pomwepo moto unatsikadi kuchokera kumwamba
ndipo unapsereza mtsogoleriyo pamodzi ndi anthu akewo.

13 Ndipo mfumu inatumanso mtsogoleri wachitatu pamodzi ndi asilikali
ake makumi asanu. Mtsogoleri wachitatuyu anakwera pa phiripo ndi
kugwada pamaso pa Eliya. Iye anayankhula mopemba kuti, “Munthu wa
Mulungu, chonde musandiwononge ineyo pamodzi ndi atumiki makumi
asanu anuwa! 14 Taonani, moto unatsika kuchokera kumwamba ndi
kupsereza atsogoleri awiri pamodzi ndi anthu awo onse. Koma tsopano
musawononge moyo wanga!”

15 Mngelo wa Yehova anati kwa Eliya, “Pita naye, usamuope.” Choncho
Eliya ananyamuka natsika naye limodzi kupita kwa mfumu.
16 Eliya anawuza mfumu kuti, “Yehova akuti, ‘Chifukwa chiyani
munatumiza amithenga kwa Baala-zebubu, mulungu wa ku Ekroni,
kukafunsa ngati muti muchire? Kodi mu Israeli mulibe Mulungu
woti n’kukuyankhani funso lanu? Choncho, popeza mwachita izi,
simudzadzuka pamene mwagonapo; mudzafa ndithu.’ ” 17 Motero Ahaziya
anafadi, monga mwa mawu a Yehova amene Eliya anayankhula.
Tsono popeza Ahaziya analibe mwana, Yoramu analowa ufumu m’malo
mwake m’chaka chachiwiri cha Yehoramu mwana wa Yehosafati mfumu
ya ku Yuda. 18 Ntchito zina zonse zimene Ahaziya anachita, kodi
sizinalembedwe m’buku la mbiri ya mafumu a ku Israeli?

# 2

*Eliya Atengedwa Kupita Kumwamba*

1 Yehova ali pafupi kutenga Eliya kupita kumwamba mu kamvuluvulu,
Eliya ndi Elisa anali pa ulendo wopita ku Giligala. 2 Eliya anawuza Elisa
kuti, “Iwe khala pano pakuti Yehova wandituma kuti ndipite ku Beteli.”
Koma Elisa anati, “Pali Yehova wamoyo ndiponso pali inu nomwe, ineyo
sindidzakusiyani.” Motero awiriwo anapita ku Beteli.
3 Ana a aneneri a ku Beteli anabwera kwa Elisa namufunsa kuti, “Kodi
ukudziwa kuti lero Yehova akuchotsera mbuye wako?”
Elisa anayankha kuti, “Inde ndikudziwa, koma musakambe zimenezi.”
4 Ndipo Eliya anati kwa Elisa, “Iwe khala pano pakuti Yehova wandituma
kuti ndipite ku Yeriko.”
Koma Elisa anayankha kuti, “Pali Yehova wamoyo ndiponso pali inu,
ineyo sindidzakusiyani.” Motero awiriwo anapita ku Yeriko.
5 Ana a aneneri amene anali ku Yeriko anapita kwa Elisa, namufunsa
kuti, “Kodi ukudziwa kuti lero Yehova akuchotsera mbuye wako?”
Elisa anayankha kuti, “Inde ndikudziwa, koma inu musakambe
zimenezi.”
6 Ndipo Eliya anati kwa Elisa, “Iwe khala pano pakuti Yehova wandituma
kuti ndipite ku Yorodani.”
Elisa anayankha kuti, “Pali Yehova wamoyo ndiponso pali inu nomwe,
ineyo sindidzakusiyani.” Motero awiriwo anapitirira ulendo wawo.
7 Anthu makumi asanu mwa ana a aneneri anawatsatira nayima
chapatali moyang’anana nawo ndipo Eliya ndi Elisa anayima m’mphepete
mwa Yorodani. 8 Eliya anatenga chovala chake nachipinda, napanda
madzi ndi chovalacho. Madziwo anagawikana, ena kwina ena kwina,
ndipo awiriwo anawoloka powuma.
9 Atawoloka, Eliya anati kwa Elisa, “Ndifotokozere, ndikuchitire chiyani
ndisanachotsedwe pamaso pako?”
Elisa anayankha kuti, “Ndikupemphani kuti mundipatse magawo awiri
a mphamvu za mzimu wanu wa uneneri.”
10 Eliya anati, “Wapempha chinthu chapatali, komabe ukandiona
pamene ndikuchotsedwa pamaso pako, mphamvu wapemphayi idzakhala
yako, koma ukapanda kundiona sizidzachitika.”
11 Akuyenda ndi kumakambirana, mwadzidzidzi galeta lamoto ndi
akavalo amoto anaonekera ndi kuwasiyanitsa awiriwo, ndipo Eliya
anapita kumwamba m’kamvuluvulu. 12 Elisa anaona zimenezi ndipo
anafuwula kuti, “Abambo anga! Abambo anga! Magaleta a Israeli ndi

anthu ake okwera pa akavalo!" Ndipo Elisa sanamuonenso Eliyayo.
Pamenepo Elisa anagwira zovala zake nazing'amba pakati.
13 Iye anatola chovala cha Eliya chomwe chinagwa nabwerera ndi
kukayima m'mphepete mwa Yorodani. 14 Ndipo Elisa anatenga chovala
chomwe chinagwa kuchokera kwa Eliya napanda nacho madzi. Iye
anafunsa kuti, "Ali kuti Mulungu wa Eliya?" Atapanda madzi, madziwo
anagawika pakati, ena kwina ena kwina, ndipo iye anawoloka.
15 Ndipo ana a aneneri ochokera ku Yeriko atamuona anati, "Mzimu wa
Eliya wakhazikika pa Elisa." Ndipo anapita kukakumana naye nagwada
ndi kuweramitsa mitu yawo pansi pamaso pake. 16 Ndipo anawuza
Elisa kuti, "Ife atumiki anu tili ndi anthu amphamvu makumi asanu.
Aloleni apite kuti akafunefune mbuye wanu. Mwina Mzimu wa Yehova
wamutenga ndi kukamuponya ku phiri lina kapena ku chigwa china."
Elisa anayankha kuti, "Ayi, musawatume."
17 Koma anamukakamizabe mpaka Elisayo anachita manyazi moti
sakanatha kukana. Choncho iye anati, "Atumizeni." Ndipo anatumiza
anthu makumi asanu amene anakafunafuna Eliya kwa masiku atatu koma
sanamupeze. 18 Atabwerera kwa Elisa (chifukwa anali akanali ku Yeriko),
iye anawawuza kuti, "Kodi sindinakuwuzeni kuti musapite?"

### *Kuchiritsidwa kwa Madzi*

19 Anthu a mu mzindamo anati kwa Elisa, "Mbuye wathu, taonani
mzinda uno uli pamalo pabwino, monga mukuoneramu, koma madzi ake
ndi oyipa, nthaka yakenso ndi yosabereka."
20 Iye anati, "Patseni mbale yatsopano ndipo muyikemo mchere." Ndipo
anabweretsa mbaleyo kwa iye.
21 Kenaka Elisa anapita ku kasupe wa madziwo, nathiramo mchere
m'kasupemo nati, "Yehova akuti, 'Ndachiritsa madzi awa. Madzi
amenewa sadzabweretsanso imfa kapena kuchititsa kuti nthaka ikhale
yosabereka.' " 22 Kotero madziwo ndi abwino mpaka lero, molingana ndi
mawu amene Elisa anayankhula.

### *Kusekedwa kwa Elisa*

23 Kuchokera kumeneko Elisa anapita ku Beteli. Ndipo pamene
ankayenda mu msewu, anyamata ena achichepere anatuluka mu mzin-
damo n'kumamuseka. Iwo ankanena kuti, "Choka iwe, wachidazi! Choka
iwe wachidazi" 24 Iye anatembenuka nawayang'ana ndipo anawatember-
era m'dzina la Yehova. Nthawi yomweyo panatulukira zimbalangondo
ziwiri kuchokera kuthengo, ndi kuphapo anyamata 42. 25 Ndipo iye
anapita ku phiri la Karimeli. Pochoka kumeneko anabwerera ku
Samariya.

## 3

### *Kuwukira kwa Mowabu*

1 Yoramu mwana wa Ahabu anakhala mfumu ya Israeli ku Samariya
m'chaka cha 18 cha Yehosafati mfumu ya ku Yuda ndipo analamulira
zaka khumi ndi ziwiri. 2 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova koma
sizinafanane ndi zimene anachita abambo ndi amayi ake. Iye anachotsa
fano la mwala la Baala limene abambo ake anapanga. 3 Komabe
anawumirira kuchita machimo a Yeroboamu mwana wa Nebati, amene
anachimwitsa nawo Israeli ndipo sanafune kuwaleka.

4 Tsono Mesa, mfumu ya ku Mowabu ankaweta nkhosa, ndipo iye
ankayenera kumapereka kwa mfumu ya ku Israeli chaka ndi chaka
ana ankhosa onenepa okwanira 100,000 pamodzi ndi ubweya wankhosa
100,000 zazimuna. 5 Koma atamwalira Ahabu, mfumu ya ku Mowabu
inawukira mfumu ya ku Israeli. 6 Choncho nthawi imeneyi mfumu Yoramu
inatuluka mu Samariya ndi kukasonkhanitsa Aisraeli onse. 7 Yoramu
anatumizanso uthenga uwu kwa Yehosafati mfumu ya ku Yuda: "Mfumu
ya ku Mowabu yandiwukira. Kodi ungapite nane kukamenyana ndi
Mowabu?"

Iye anayankha kuti, "Ine ndidzapita nawe. Iwe ndi ine ndife anthu amodzi, anthu anga ali ngati anthu ako, akavalo anga ali ngati akavalo ako."

8 Yehosafati anafunsa kuti, "Kodi tidzera njira iti popita ku nkhondoko?"

Yoramu anayankha kuti, "Tidzera ku Chipululu cha Edomu."

9 Choncho mfumu ya ku Israeli inanyamuka pamodzi ndi mfumu ya ku Yuda ndi ya ku Edomu. Ndipo atayenda mozungulira m'chipululu kwa masiku asanu ndi awiri, asilikali analibe madzi woti amwe kapena kumwetsa nyama zawo zosenza katundu.

10 Mfumu inafuwula kuti, "N'chiyani chomwe chikutichitikira! Kodi Yehova wasonkhanitsa mafumu atatu pamodzi kuti atipereke m'manja mwa Amowabu?"

11 Koma mfumu Yehosafati inafunsa kuti, "Kodi kuno kulibe mneneri wa Yehova woti tingakafunse kwa Yehova kudzera mwa iyeyo?"

Mtsogoleri wa ankhondo wa mfumu ya ku Israeli anayankha kuti, "Alipo, Elisa mwana wa Safati. Iye anali mtumiki wa Eliya."

12 Yehosafati anati, "Yehova amayankhula kudzera mwa iye." Choncho mfumu ya ku Israeli pamodzi ndi Yehosafati ndiponso mfumu ya ku Edomu anapita kwa Elisa.

13 Elisa ananena kwa mfumu ya ku Israeli kuti, "Pali ubale wanji pakati pa inu ndi ine? Pitani kwa aneneri a abambo ndi amayi anu."

Mfumu ya ku Israeli inayankha kuti, "Ayi, pakuti ndi Yehova amene anatisonkhanitsa ife mafumu atatu pamodzi kuti atipereke m'manja mwa Amowabu."

14 Elisa anati, "Pali Yehova Wamphamvuzonse amene ndimamutu-
mikira, pakanapanda kuti ndimamuchitira ulemu Yehosafati mfumu ya ku
Yuda, sindikanakulabadirani kapena kukuyang'anani n'komwe. 15 Koma
tsopano ndiyitanireni munthu wodziwa kuyimba bwino zeze."

Munthuyo akuyimba zeze, mphamvu ya Yehova inafika pa Elisa,
16 ndipo anati, "Yehova akuti, 'Kumbani ngalande m'chigwa chonse.'
17 Pakuti Yehova akunena kuti, 'Simudzaona mphepo kapena mvula,
komabe chigwa ichi chopanda madzi chidzadzaza ndi madzi, ndipo inu
mudzamwa pamodzi ndi ng'ombe zanu ndiponso nyama zanu zonse.'
18 Izi ndi zosavuta pamaso pa Yehova. Ndipo adzaperekanso Amowabu
m'manja mwanu. 19 Mudzagonjetsa mizinda yawo yonse yotetezedwa
ndiponso mizinda yawo ikuluikulu. Mudzagwetsa mtengo wabwino
uliwonse, mudzatseka akasupe onse amadzi, ndiponso mudzawononga
minda yawo yonse yachonde poponyamo miyala."

20 Mmawa mwake, nthawi yopereka nsembe ili pafupi, anangoona madzi akutuluka kuchokera ku Edomu, ndipo malo onse anadzaza ndi madzi.

21 Tsono n'kuti Amowabu onse atamva kuti mafumu abwera kudzachita nawo nkhondo. Kotero, anayitana munthu aliyense, wamkulu ndi

wamng’ono amene ankatha kugwira chida chankhondo ndipo anakayima
ku malire a dziko lawo. 22 Amowabu atadzuka mmamawa, dzuwa
likuwala pa madziwo, anaona madziwo akuoneka wofiira ngati magazi
patsogolo pawo. 23 Ndipo iwo anati, “Taonani magazi! Mafumu aja
amenyana okhaokha ndipo aphana. Amowabu, tsopano ndi nthawi
yofunkha!”

24 Koma Amowabu atafika ku misasa ya Israeli, Aisraeli ananyamuka ndi
kumenyana nawo mpaka anathawa. Ndipo Aisraeli analowa m’dzikolo
ndi kupha Amowabu. 25 Aisraeli anagumula mizinda yawo ndipo munthu
aliyense anaponya mwala pa munda uliwonse wachonde mpaka utadzaza
ndi miyala. Iwo anatseka akasupe onse amadzi ndiponso anadula mtengo
wabwino uliwonse. Mzinda wa Kiri Hareseti wokha ndiye unatsala
wotetezedwa koma anthu oponya miyala anawuzungulira nawuthiranso
nkhondo.

26 Mfumu ya ku Mowabu itaona kuti nkhondo ikumulaka, inatenga
anthu 700 a malupanga kuti athawe modutsa mfumu ya ku Edomu, koma
inalephera. 27 Choncho inatenga mwana wake wamwamuna woyamba
kubadwa, amene akanalowa ufumu m’malo mwake, ndi kumupereka
nsembe pa khoma la mzinda. Zimenezi zinachititsa kuti mkwiyo ndi ukali
wa Amowabu ukule kwambiri pa Aisraeli ndipo Aisraeliwo anathawa
nabwerera ku dziko la kwawo.

# 4

### *Mafuta a Mkazi Wamasiye*

1 Mkazi wa mmodzi mwa ana a aneneri anafuwula kwa Elisa kuti,
“Mtumiki wanu, mwamuna wanga wamwalira ndipo inu mukudziwa
kuti ankaopa Yehova. Koma tsopano munthu amene mwamuna wanga
anakongolako zinthu zake, akubwera kudzatenga ana anga awiri aamuna
kuti akhale akapolo ake.”

2 Elisa anayankha mayiyo kuti, “Kodi ufuna ndikuchitire chiyani?
Tandiwuza uli ndi chiyani m’nyumba mwako?”

Mayiyo anayankha kuti, “Mdzakazi wanu alibe kanthu kalikonse koma
timafuta pang’ono chabe.”

3 Elisa anati, “Pita kabwereke mitsuko yonse yopanda kanthu
kwa anzako. Usakabwereke mitsuko yochepa. 4 Kenaka ukalowe
m’nyumba mwako ndi kudzitsekera iwe ndi ana ako. Mukakatero
mukakhuthulire mafuta m’mitsuko yonseyo, ndipo mtsuko uliwonse
ukadzaza muzikawuyika pambali.”

5 Mayi uja anachoka kwa Elisa nakadzitsekera ndi ana ake. Anthu
anabweretsa mitsuko kwa iye ndipo ankathiramo mafuta. 6 Mitsuko yonse
itadzaza, mayiyo anawuza mwana wake kuti, “Bweretsa mtsuko wina.”

Koma iye anayankha kuti, “Mitsuko yonse yatha.” Pamenepo mafuta
analeka kutuluka.

7 Mayiyo anapita nakamuwuza munthu wa Mulungu amene ana-
muyankha kuti, “Pita, kagulitse mafutawo ndipo ukabweze ngongole ija.
Ndalama zotsalazo zikakhale zako ndi ana ako.”

### *Elisa Aukitsa Mwana wa Mayi wa ku Sunemu*

8 Tsiku lina Elisa anapita ku Sunemu. Kumeneko kunkakhala mayi
wina wachuma amene anawumiriza Elisa kuti adye chakudya. Choncho
nthawi iliyonse imene Elisa amadutsa kumeneko, ankayima ndi kudya.
9 Mayiyo anawuza mwamuna wake kuti, “Taonani, ine ndikudziwa kuti

munthu amene amadutsa pano nthawi zambiriyu ndi munthu woyera
wa Mulungu. 10 Tiyeni timumangire kachipinda kakang'ono pa denga
la nyumbayi ndi kumuyikiramo bedi ndi tebulo, mpando ndi nyale.
Akabwera kuno azikhala m'menemo."
11 Tsiku lina pamene Elisa anafika ku Sunemu, iye anakalowa
m'chipinda chake chija nagona m'menemo. 12 Iye anati kwa mtumiki
wake Gehazi, "Muyitane Msunemuyu." Ndipo anapita kukamuyitana
mayiyo, ndipo anabwera nayima pamaso pa Elisa. 13 Elisa anati kwa
Gehazi, "Muwuze mayiyo kuti, 'Wavutika potichitira zonsezi. Nanga
tsopano ifeyo tikuchitire chiyani? Kodi ukufuna kuti tikadziwitse mfumu
kapena mtsogoleri wa ankhondo zimene watichitirazi?' "

Mayiyo anayankha kuti, "Ine ndimakhala mwamtendere pakati pa abale
anga."

14 Elisa anafunsanso Gehazi kuti, "Kodi tingamuchitire chiyani?"

Gehazi anati, "Ndithu, mayiyu alibe mwana ndipo mwamuna wake ndi
wokalamba."

15 Pamenepo Elisa anati, "Muyitane." Choncho Gehazi anamuyitana,
ndipo iye anabwera nayima pa khomo. 16 Elisa anati kwa mayiyo,
"Nthawi ngati yomwe ino chaka chamawa, udzakhala utanyamula mwana
wamwamuna m'manja mwako."

Mayiyo anatsutsa zimenezi nanena kuti, "Ayi mbuye wanga. Inu
munthu wa Mulungu, musanamize mdzakazi wanu!"

17 Koma mayi uja anakhala woyembekezera, ndipo chaka chotsatiracho,
nthawi ngati yomweyo anabereka mwana wamwamuna monga momwe
Elisa anamuwuzira.

18 Mwana uja anakula, ndipo tsiku lina anapita kwa abambo ake amene
anali ndi anthu odula tirigu. 19 Mwanayo anafuwula kwa abambo ake kuti,
"Mayo! Mutu wanga ine! Mayo! Mutu wanga ine!"

Abambo akewo anawuza wantchito wake kuti, "Munyamule ndi
kukamupereka kwa amayi ake." 20 Wantchito uja atamunyamula ndi
kumupereka kwa amayi ake. Mwanayo anakhala pa miyendo ya amayi
akeyo mpaka masana, ndipo pambuyo pake anamwalira. 21 Mayiyo
ananyamula mwanayo nakamugoneka pa bedi la munthu wa Mulungu
uja. Kenaka anatseka chitseko iye n'kuchokapo.

22 Iye anayitanitsa mwamuna wake namuwuza kuti, "Tumizireni
wantchito mmodzi ndi bulu mmodzi kuti ndipite mofulumira kwa munthu
wa Mulungu n'kubwererako."

23 Mwamuna wakeyo anafunsa kuti, "Chifukwa chiyani ukupita kwa
iyeyo lero? Lero si tsiku la Chikondwerero cha Mwezi Watsopano kapena
tsiku la Sabata."

Mayiyo anayankha kuti, "Zonse zili bwino."

24 Mayiyo anamangirira chishalo pa bulu ndipo anawuza wantchito
wake kuti, "Yendetsa bulu mofulumira. Usachepetse liwiro pokhapokha
nditakuwuza." 25 Choncho ananyamuka nakafika kwa munthu wa
Mulungu uja ku Phiri la Karimeli.

Munthu wa Mulungu ataona mayiyo patali, anawuza mtumiki wake
Gehazi kuti, "Taona! Msunemu uyo! 26 Thamanga msanga ukakumane
naye ndipo ukamufunse kuti, 'Kodi muli bwino? Kodi mwamuna wanu
ali bwino? Kodi mwana wanu ali bwino?' "

Mayiyo anayankha kuti, "Zonse zili bwino."

27 Atafika kwa munthu wa Mulunguyo pa phiripo, mayiyo anagwira
mapazi a Elisa. Gehazi anabwera kuti amukankhe, koma munthu wa

Mulungu anati, “Musiye! Iyeyu ali pa mavuto aakulu, koma Yehova wandibisira zimenezi ndipo sanandiwuze chifukwa chake.”
28 Tsono mayiyo anati, “Mbuye wanga, kodi ine ndinakupemphani mwana? Kodi sindinakuwuzeni kuti musandinamize?”
29 Elisa anawuza Gehazi kuti, “Manga lamba m’chiwuno mwako, tenga ndodo yanga m’dzanja lako ndipo thamanga. Ngati ukumana ndi munthu wina aliyense, usamupatse moni, ndipo ngati wina akupatsa moni, usayankhe. Ukagoneke ndodo yanga pa nkhope ya mwanayo.”
30 Koma mayi wake wa mwana uja anati, “Pali Yehova wamoyo ndiponso pali inu nomwe, ineyo sindidzakusiyani.” Choncho Elisa ananyamuka natsatira mayiyo.
31 Gehazi anatsogola nakagoneka ndodoyo pa nkhope ya mwanayo, koma sipanamveke mawu kapena kugwedezeka kuonetsa kuti ali moyo. Choncho Gehazi anabwerera kukakumana ndi Elisa ndipo anamuwuza kuti, “Mwanayo sanatsitsimuke.”
32 Ndipo Elisa atafika ku nyumbako, taonani, mwanayo anali wakufa
atamugoneka pa bedi lake. 33 Elisa analowa m’nyumbamo natseka
chitseko. Anali awiri okha m’chipindamo ndipo iye anapemphera
kwa Yehova. 34 Kenaka anakwera pa bedi ndi kumugonera mwanayo,
pakamwa pake panakhudzana ndi pakamwa pa mwanayo, maso ake
anakhudzana ndi maso a mwanayo, ndipo manja ake anakhudzana ndi
manja a mwanayo. Pamene ankadzitambalitsa yekha pa mwanayo, thupi
la mwanayo linayamba kufunda. 35 Elisa anatembenuka nayenda uku
ndi uku kamodzi m’chipindamo ndipo kenaka anakweranso pa bedi
nagoneranso mwanayo. Mwanayo anayetsemula kasanu ndi kawiri ndipo
anatsekula maso ake.
36 Elisa anayitana Gehazi ndipo anati, “Muyitane Msunemuyo.” Ndipo
anaterodi. Mayiyo atabwera, Elisa anati, “Tenga mwana wako.” 37 Mayiyo
analowa, nagwada pa mapazi a Elisa, naweramitsa mutu wake pansi.
Kenaka ananyamula mwana wake natuluka.

### *Imfa mu M’phika*

38 Elisa anabwerera ku Giligala ndipo ku dera limenelo kunali njala. Elisa akukumana ndi ana a aneneri, anati kwa mtumiki wake, “Ika m’phika waukulu pa moto ndipo uwaphikire chakudya anthu awa.”
39 Mmodzi mwa ana aneneriwo anapita kuthengo kukafuna ndiwo ndipo
anakapeza mpesa wakuthengo. Iye anathyolako zipatso zake nadzaza
nsalu yake. Atabwerera, anazidula zipatsozo naziyika mu m’phika,
ngakhale kuti panalibe amene ankazidziwa. 40 Anawapakulira anthu
chakudyacho, koma atayamba kudya, anthuwo anafuwula kuti, “Inu
munthu wa Mulungu muli imfa mu m’phikamu!” Ndipo sakanatha kudya
chakudyacho.
41 Elisa anati, “Bweretsani ufa.” Iye anathira ufa mu m’phikamo ndipo anati, “Perekani chakudyachi kwa anthu kuti adye.” Ndipo mu m’phikamo munalibenso zoopsa.

### *Kudyetsa Anthu 100*

42 Munthu wina wochokera ku Baala-Salisa anabwera atamutengera munthu wa Mulungu malofu a barele makumi awiri opangidwa kuchokera ku zokolola zoyamba kucha, pamodzinso ndi ngala zatsopano za tirigu. Elisa anati kwa munthuyo, “Apatse anthu kuti adye.”
43 Mtumiki wake anafunsa kuti, “Kodi ndikachigawe motani chakudyachi kwa anthu 100?”

Koma Elisa anamuwuzanso kuti, “Apatse anthu adye. Pakuti izi ndi
zimene Yehova akunena kuti, ‘Iwo adzadya chakudyachi ndipo china
chidzatsalako.’ ” 44 Tsono iye anachipereka kwa anthuwo ndipo anadya
china n’kutsalako, molingana ndi mawu a Yehova.

# 5

*Naamani Achiritsidwa Khate Lake*

1 Tsono Naamani anali mtsogoleri wa gulu lankhondo a mfumu ya
ku Aramu. Iye anali munthu wodalirika pamaso pa mbuye wake
ndipo anali wokondedwa kwambiri, chifukwa kudzera mwa iye Yehova
anapambanitsa Aaramu. Anali msilikali wolimba mtima, koma anali ndi
khate.

2 Tsono magulu a Aaramu anapita ku nkhondo ndipo anakagwira
ukapolo mtsikana wamng’ono wa ku Israeli, ndipo ankatumikira mkazi
wa Naamani. 3 Mtsikanayo anawuza mkazi wa Naamani kuti, “Mbuye
wanga akanapita kukaonana ndi mneneri amene amakhala ku Samariya,
akanachiritsidwa khate lawo.”

4 Naamani anapita kwa mbuye wake kukamuwuza zomwe mtsikana
wochokera ku Israeli ananena. 5 Mfumu ya ku Aramu inayankha kuti,
“Iwe uyenera kupita. Ine ndilembera kalata mfumu ya ku Israeli.”
Choncho Naamani ananyamuka kupita ku Samariya, atatenga ndalama
za siliva 30,000, ndalama zagolide 6,000 ndiponso zovala khumi za pa
chikondwerero. 6 Kalata imene anapita nayo kwa mfumu ya ku Israeli
inali ndi mawu awa: “Taonani, ndikutumiza Naamani mtumiki wanga
pamodzi ndi kalatayi kwa inu kuti mumuchiritse khate lake.”

7 Mfumu ya ku Israeli itangowerenga kalatayo, inang’amba mkanjo
wake ndipo inati, “Kodi ine ndine Mulungu? Kodi ndingathe kupha
kapena kupereka moyo? Chifukwa chiyani munthu ameneyu wanditu-
mizira munthu woti ndimuchiritse khate lake? Taonani, iyeyu akungofuna
kuti apeze chifukwa choyambanirana nane!”

8 Elisa munthu wa Mulungu atamva kuti mfumu ya ku Israeli yang’amba
mkanjo wake, anatumiza uthenga uwu: “Chifukwa chiyani mwang’amba
mkanjo wanu? Mutumizeni munthuyo kwa ine ndipo iyeyo adzadziwa
kuti muli mneneri mu Israeli.” 9 Choncho Naamani anapita pamodzi ndi
akavalo ake ndi magaleta nakayima pa khomo la nyumba ya Elisa. 10 Elisa
anatumiza uthenga kwa iye woti, “Pita, kasambe kasanu ndi kawiri mu
mtsinje wa Yorodani, thupi lako lidzachira ndi kukhalanso monga kale
ndipo udzayeretsedwa.”

11 Koma Naamani anachoka mokwiya ndipo anati, “Ine ndimaganiza
kuti munthuyu atuluka ndipo ayimirira nayitana dzina la Yehova Mulungu
wake, nayendetsa dzanja lake pamwamba pa nthendayi ndi kundichiritsa
khate langa. 12 Kodi Abana ndi Faripara, mitsinje ya ku Damasiko,
siyoposa mitsinje ina yonse ya ku Israeli? Kodi sindikanasamba m’mitsinje
imeneyo ndi kuyeretsedwa?” Kotero anatembenuka nachoka ali wokwiya
kwambiri.

13 Antchito ake anamuyandikira namufunsa kuti, “Abambo anga,
mneneri akanakulamulani chinthu chachikulu, kodi inu simukanachita?
Nanga n’zovuta motani zomwe mneneri wanena kuti ‘Kasambeni ndipo
mudzayeretsedwa!’ ” 14 Choncho Naamani anapita ku Yorodani nakadz-
imiza m’madzimo kasanu n’kawiri, monga momwe munthu wa Mulungu
anamuwuzira. Thupi lake linakhalanso monga kale ndipo linakhala
losalala ngati la kamnyamata.

15 Pamenepo Naamani ndi atumiki ake onse anabwerera kwa munthu
wa Mulungu uja. Naamani anayima pamaso pa Elisa ndipo anati,
“Tsopano ndikudziwa kuti kulibe Mulungu wina pa dziko lonse lapansi
koma mu Israeli mokha. Chonde, tsopano landirani mphatso ya mtumiki
wanu.”
16 Mneneri anayankha kuti, “Pali Yehova wamoyo, amene ine ndi-
mamutumikira, sindidzalandira zimenezi.” Ndipo ngakhale Naamani
anamukakamiza, iye anakanabe.
17 Naamani anati, “Ngati inu simulandira, chonde lolani mtumiki wanu
kuti atengeko dothi lokwanira kunyamula abulu awiri, popeza mtumiki
wanu sadzaperekanso nsembe yopsereza ndi nsembe zina kwa mulungu
wina koma Yehova. 18 Koma Yehova andikhululukire ine pa chinthu ichi:
Pamene mbuye wanga alowa m’nyumba ya mapemphero ya Rimoni ine
ndimapita naye ndipo ndimakagwada naye limodzi. Pamene ndikugwada
m’nyumba ya mapemphero ya Rimoni, Yehova azikhululukira mtumiki
wanu pa chinthu chimenechi.”
19 Elisa anati, “Pita mu mtendere.”
Choncho anachoka nayenda pang’ono. 20 Koma Gehazi, mtumiki wa
Elisa munthu wa Mulungu, anaganiza mu mtima mwake kuti, “Taonani,
mbuye wanga wamulekerera Naamani Mwaramuyu, posalandira zomwe
anabweretsa. Pali Yehova wamoyo, ine ndimuthamangira ndipo ndikaten-
gako zinthu kwa iye.”
21 Choncho Gehazi anamuthamangira Naamani uja. Naamani ataona
Gehazi akumuthamangira, anatsika m’galeta lake ndi kukakumana naye.
Iye anafunsa Gehazi kuti, “Kodi n’kwabwino?”
22 Gehazi anayankha kuti, “Inde n’kwabwino. Mbuye wanga wandi-
tuma kuti ndidzakuwuzeni kuti, ‘Anyamata awiri mwa ana a aneneri
angondipeza kumene kuchokera ku dziko la mapiri la Efereimu. Chonde
apatseniko ndalama za siliva 3,000 ndi zovala ziwiri za pa phwando.’ ”
23 Naamani anati, “Kuli bwino utenge ndalama zasiliva 6,000.” Iye
anakakamiza Gehazi kuti alandire, ndipo kenaka anamanga matumba
awiri a ndalama zasiliva pamodzi ndi zovala zinayi za pa mphwando. Naa-
mani anazipereka kwa antchito ake awiri ndipo anazinyamula nayenda
patsogolo pa Gehazi. 24 Gehazi atafika ku phiri, anawalanda antchito
aja zinthu zija nazibisa m’nyumbamo. Iye anawawuza anthu aja kuti
abwerere ndipo anapita. 25 Kenaka analowa m’nyumbamo nakayima
pamaso pa mbuye wake Elisa.
Elisa anafunsa kuti, “Kodi Gehazi unali kuti?”
Iye anayankha kuti, “Mtumiki wanu sanapite kwina kulikonse.”
26 Koma Elisa anati kwa Gehazi, “Kodi mzimu wanga sunali nawe
pamene munthu uja anatsika m’galeta lake ndi kukumana nawe? Kodi
ino ndi nthawi yolandira ndalama, kapena kulandira zovala, mitengo ya
olivi, minda ya mpesa, nkhosa, ng’ombe kapena antchito aamuna kapena
antchito aakazi? 27 Khate la Naamani lidzakumatirira iwe ndi zidzukulu
zako mpaka muyaya.” Ndipo Gehazi anachoka pamaso pa Elisa ali ndi
khate lotuwa ngati phulusa.

# 6

*Nkhwangwa Iyandama pa madzi*

1 Ana a aneneri anati kwa Elisa, “Taonani malo amene timakhala ndi
inu atichepera kwambiri. 2 Tiloleni tipite ku Yorodani kumene aliyense
wa ife akadule mtengo umodzi, kuti timange malo woti tizikhalamo.”

Ndipo Elisa anati, “Pitani.”

3 Mmodzi wa iwo anati, “Chonde mulole kutsagana nawo atumiki anu.”

Elisa anayankha kuti, “Ndipita nanu.” 4 Ndipo anapita nawo.

Anapita ku Yorodani nayamba kudula mitengo. 5 Pamene wina ankadula
mtengo, nkhwangwa yake inaguluka nigwera m’madzi. Iye anafuwula
kuti, “Mayo! Mbuye wanga! Popeza ndi yobwereka!”

6 Ndipo munthu wa Mulungu uja anafunsa, “Yagwera pati?” Pamene
anamuonetsa malowo, Elisa anadula kamtengo nakaponya pamenepo,
ndipo nkhwangwayo inayandama. 7 Elisa anati, “Itenge.” Ndipo
munthuyo anatambalitsa dzanja lake nayitenga.

### *Elisa Achititsa Khungu Ankhondo a ku Aramu*

8 Tsono mfumu ya ku Aramu inali pa nkhondo ndi Israeli. Itakambirana
ndi atsogoleri ake ankhondo inati, “Ndidzamanga misasa yanga pamalo
akutiakuti.”

9 Munthu wa Mulungu anatumiza mawu kwa mfumu ya ku Israeli kuti
“Musamale podutsa malo akuti, chifukwa Aaramu akupita kumeneko.”
10 Choncho mfumu ya ku Israeli inatuma anthu kumalo kumene munthu
wa Mulunguyo ananena. Nthawi ndi nthawi Elisa ankachenjeza mfumu,
kotero kuti ankakhala tcheru ku malo amenewo.

11 Zimenezi zinakwiyitsa kwambiri mfumu ya ku Aramu. Mfumuyo
inayitanitsa atsogoleri ake ankhondo ndipo inawafunsa kuti, “Kodi
simungandiwuze munthu amene pakati pathu pano ali mbali ya mfumu
ya ku Israeli?”

12 Mmodzi mwa atsogoleri a ankhondowo anati, “Palibe ndi mmodzi
yemwe pakati pathu, inu mbuye wanga, koma Elisa mneneri amene
ali ku Israeli amawuza mfumu ya ku Israeli mawu enieni amene inu
mumayankhula ku chipinda kwanu.”

13 Choncho mfumu inalamula kuti, “Pitani, kafufuzeni kumene akukhala
kuti ine ndditume anthu kukamugwira.” Anthuwo anabweretsa mawu
oti, “Taonani, Elisa ali ku Dotani.” 14 Ndipo mfumu inatumizako
magaleta ndi akavalo ndiponso gulu lankhondo lamphamvu. Anapita
usiku nakawuzungulira mzindawo.

15 Mtumiki wa munthu wa Mulungu atadzuka mmamawa ndi kutuluka
panja, gulu la ankhondo pamodzi ndi akavalo ndi magaleta anali atazun-
gulira mzindawo. Mtumikiyo anafunsa kuti, “Kalanga mbuye wanga,
tidzachita chiyani?”

16 Mneneri anamuyankha kuti, “Usachite mantha. Amene ali mbali
yathu ndi ambiri kupambana amene ali mbali yawo.”

17 Ndipo Elisa anapemphera kuti, “Inu Yehova tsekulani maso ake
kuti aone.” Pamenepo Yehova anatsekula maso a mtumikiyo, ndipo
anayang’ana naona kuti phiri lonse linali lodzaza ndi akavalo ndi
magaleta a moto atazungulira Elisa.

18 Pamene adaniwo ankabwera kudzalimbana naye, Elisa anapemphera
kwa Yehova kuti, “Achititseni khungu anthu awa.” Kotero Yehova
anawachititsa khungu monga anapemphera Elisa.

19 Elisa anawawuza ankhondowo kuti, “Njira si imeneyi ndipo mzinda
sumenewunso. Tsateni, ndipo ndidzakutengerani kwa munthu amene
mukumufunayo.” Ndipo anawatengera ku Samariya.

20 Atalowa mu mzinda wa Samariya, Elisa anati, “Yehova tsekulani maso
a anthu awa kuti aone.” Choncho Yehova anatsekula maso awo ndipo
anangoona kuti ali m’kati mwenimweni mwa Samariya.

21 Mfumu ya ku Israeli itawaona, inafunsa Elisa kuti, “Abambo anga,
kodi ndiwaphe? Kodi ndiwaphe?”

22 Elisa anayankha kuti, “Musawaphe. Kodi mungaphe anthu amene
munawagwira pogwiritsa ntchito lupanga ndi uta? Apatseni chakudya ndi
madzi kuti adye ndi kumwa kenaka apite kwa mbuye wawo.” 23 Choncho
anawakonzera mphwando lalikulu, ndipo atatsiriza kudya ndi kumwa,
anawatumiza kwawo ndipo anabwerera kwa mbuye wawo. Kotero
magulu a ankhondo a ku Aramu analeka kuthira nkhondo dziko la Israeli.

### *Njala mu Mzinda wa Samariya*

24 Patapita nthawi, Beni-Hadadi mfumu ya Aramu anasonkhanitsa gulu
lake lonse la ankhondo, napita kukazungulira mzinda wa Samariya. 25 Mu
mzinda wa Samariya munali njala yoopsa. Ndipo taonani, Aaramu
anazungulira mzindawu kwa nthawi yayitali kotero kuti mutu wa bulu
ankawugulitsa ndalama za siliva 80, ndipo magalamu 200 a zitosi za
nkhunda ankawagulitsa pa mtengo wa masekeli asanu.

26 Pamene mfumu inkayenda pa khoma la mzindawo, mayi wina
anafuwulira mfumuyo kuti, “Thandizeni mbuye wanga mfumu!”

27 Mfumu inayankha kuti, “Ngati Yehova sakuthandiza iwe, ine thandizo
lako ndingalipeze kuti? Kuchokera ku malo opunthira tirigu kodi?
Kuchokera kumalo opsinyira mphesa kodi?” 28 Pamenepo mfumuyo
inafunsa mayiyo kuti, “Kodi chakuvuta n’chiyani?”

Iye anayankha kuti, “Mayi uyu anandiwuza kuti, ‘Bweretsa mwana
wako kuti timudye lero, ndipo mawa tidzadya mwana wangayu.’
29 Choncho tinaphika mwana wanga ndi kumudya. Tsiku lotsatira lakelo
ine ndinati, ‘Bweretsa mwana wako kuti timudye,’ koma iye anabisa
mwana wakeyo.”

30 Mfumu itamva mawu a mayiyo, inang’amba mkanjo wake. Pamene
inkayenda pa khoma, anthu anayang’ana, ndipo anaona zovala zam’kati,
pakuti anavala chiguduli. 31 Mfumuyo inati, “Mulungu andilange,
andilange kwambiri ndikapanda kudula mutu wa Elisa mwana wa Safati
lero!”

32 Tsono Elisa n’kuti atakhala m’nyumba mwake, ndipo akuluakulu anali
naye limodzi. Mfumu inatuma munthu wina kuti imutsogolere, koma
asanafike, Elisa anawuza akuluakuluwo kuti, “Kodi simukuona momwe
wopha munthu uja watumizira munthu wina kuti adzadule mutu wanga?
Taonani mthengayo akafika, mutseke chitseko ndipo muchigwiritsitse kuti
asalowe. Kodi ndikumvawo pambuyo pake si mgugu wa mbuye wake?”

33 Elisa akuyankhulabe ndi anthuwo, taonani, wamthengayo anafika
kwa iye. Ndipo mfumu inati, “Mavuto amenewa ndi ochokera kwa Yehova.
Kodi n’chifukwa chiyani ine ndiyenera kudikira thandizo lochokera kwa
Yehova?”

# 7

1 Ndipo Elisa anati, “Mverani mawu a Yehova. Yehova akuti, ‘Mawa
nthawi ngati yomwe ino, makilogalamu atatu a ufa adzawagulitsa pa
mtengo wa ndalama imodzi yasiliva, ndipo makilogalamu asanu ndi
limodzi a barele adzawagulitsa pa mtengo wa ndalama imodzi yasiliva
ku chipata cha Samariya.’ ”

2 Mtsogoleri amene mfumu inkamudalira anati kwa munthu wa Mu-
lungu, “Taona, ngakhale Yehova atatsekula zipata zakumwamba, kodi
zimenezi zingachitikedi?”

Elisa anamuyankha kuti, “Taona, iweyo udzaziona zimenezi ndi maso ako, koma sudzadyako kanthu.”

### *Akhate Anayi Awulula za Kuthawa kwa Aaramu*

3 Tsono pa chipata cholowera mu mzinda wa Samariya pankakhala
anthu anayi akhate. Iwo anayankhulana kuti, “Chifukwa chiyani tikun-
gokhala pano kudikira kufa? 4 Ngati tinganene kuti, ‘Tidzalowa mu
mzinda,’ njala ili mu mzindamo ndipo tidzafa. Ndipo ngati tikhalebe
pano, tidzafa ndithu. Choncho tiyeni tipite ku msasa wa Aaramu ndi
kukadzipereka. Ngati sakatipha, tidzakhala ndi moyo, ngati akatipha, basi
tikafa.”
5 Iwo ananyamuka ndi kachisisira kupita ku msasa wa Aaramu. Atafika
m’malire a msasa, taonani, sanapeze munthu ndi mmodzi yemwe, 6 pakuti
Ambuye anali atamveketsa phokoso la magaleta ndi akavalo ndiponso
mdidi wa gulu lalikulu la ankhondo, kotero anayamba kuwuzana kuti,
“Taonani, mfumu ya ku Israeli yalemba ganyu mafumu a Ahiti ndi a
Aigupto kuti adzatithire nkhondo!” 7 Choncho ananyamuka nathawa ndi
kachisisira ndipo anasiya matenti, akavalo ndi abulu awo. Iwo anasiya
msasa wawo momwe unalili nathawa kupulumutsa miyoyo yawo.
8 Anthu akhate aja atafika m’malire mwa msasa analowa m’tenti imodzi.
Anadya ndi kumwa, natenga siliva, golide ndi zovala ndipo anachoka
kupita kukazibisa. Atabwerera anakalowa m’tenti ina ndipo anatenga
zinthu m’menemo nakazibisanso.
9 Kenaka akhate aja anawuzana kuti, “Ife sitikuchita bwino. Lero ndi
tsiku la uthenga wabwino ndipo tikungokhala chete. Tikadikira mpaka
kucha, tidzalangidwa. Tiyeni msanga tikafotokoze zimenezi ku nyumba
yaufumu.”
10 Choncho anapita nakayitana alonda a pa chipata cha mzinda ndi
kufotokoza kuti, “Ife tinapita ku msasa wa Aaramu ndipo sitinapezeko
munthu, kapena phokoso la wina aliyense koma tinangopeza akavalo okha
pamodzi ndi abulu ali chimangire.” 11 Alonda a pa chipata aja analengeza
uthengawu kwa okhala m’nyumba yaufumu.
12 Mfumu inadzuka usiku ndipo inawuza atsogoleri ake a ankhondo
kuti, “Ndikukuwuzani zimene Aaramu atichitira ife. Akudziwa kuti tikufa
ndi njala; kotero achoka mu msasa wawo kukabisala kuthengo ndi kuti,
‘Iwowa atuluka ndithu, ndipo ife tidzawagwira amoyo ndi kulowa mu
mzindamo.’ ”
13 Mmodzi mwa atsogoleri ake ankhondo anayankha kuti, “Chonde
uzani anthu ena atenge akavalo asanu amene atsala mu mzinda muno.
Taonani, zomwe zingawachitikire zidzakhala zofanana ndi zomwe zinga-
chitikire ena onse amene atsala. Inde iwo adzangokhala ngati Aisraeli ena
onse amene awonongeka kale. Choncho tiyeni tiwatume akafufuze zomwe
zachitika.”
14 Choncho anasankha magaleta awiri pamodzi ndi akavalo ake, ndipo
mfumu inawatuma kuti alondole gulu lankhondo la Aaramu. Mfumuyo
inalamula oyendetsa akavalowo kuti, “Pitani kaoneni.” 15 Anthuwa
anawalondola mpaka ku Yorodani, ndipo taonani, m’njira monse mu-
nali zovala zokhazokha ndi zinthu zimene Aaramu ankazitaya pamene
ankathawa mofulumira. Ndipo amithengawo anabwerera ndi kudzafo-
tokozera mfumu. 16 Tsono anthu a mu Samariya anatuluka nakafunkha ku
msasa wa Aaramu. Kotero kuti makilogalamu atatu a ufa ankawagulitsa
pa mtengo wa ndalama imodzi yasiliva, ndipo makilogalamu asanu ndi

limodzi a barele ankawagulitsanso pa mtengo wa ndalama imodzi yasiliva, monga momwe ananenera Yehova.
[17] Tsono mfumu inayika mtsogoleri amene ankamudalira uja kuti akhale woyang'anira pa chipata ndipo anthu anamupondaponda ku chipata kuja, ndipo anafa, monga momwe Elisa munthu wa Mulungu ananenera
mfumu itapita ku nyumba yake. [18] Zinachitika molingana ndi zomwe ananena munthu wa Mulungu zija kuti "Mawa nthawi ngati yomwe ino, makilogalamu atatu a ufa adzawagulitsa pa mtengo wa ndalama imodzi yasiliva ndipo makilogalamu asanu ndi limodzi a barele adzawagulitsa pa mtengo wa ndalama imodzi yasiliva ku chipata cha Samariya."
[19] Mtsogoleriyu ananena kwa munthu wa Mulungu kuti, "Taona, ngakhale Yehova atatsekula zipata zakumwamba, kodi zimenezi zingachitikedi?" Munthu wa Mulungu anamuyankha kuti, "Iwe udzaziona
zimenezi ndi maso ako, koma sudzadyako kanthu." [20] Ndipo izi ndi
zomwe zinamuchitikiradi mtsogoleriyu, pakuti anthu anamupondaponda pa chipata ndipo anafa.

# 8

*Mayi wa ku Sunemu Atenganso Munda wake*

[1] Ndipo Elisa anawuza mayi amene anamuukitsira mwana wake kuti, "Choka kuno pamodzi ndi banja lako ndipo ukakhale kulikonse ukufuna, chifukwa Yehova akubweretsa njala ya zaka zisanu ndi ziwiri m'dziko
muno." [2] Mayiyo ananyamuka nachita zimene munthu wa Mulungu ananena. Iye pamodzi ndi banja lake anachoka nakakhala ku dziko la Afilisti zaka zisanu ndi ziwiri.
[3] Zitatha zaka zisanu ndi ziwirizo anabwera kuchokera ku dziko la Afilisti ndipo anapita kwa mfumu kukafunsa za nyumba yake ndi munda
wake. [4] Ndipo mfumu inkayankhula ndi Gehazi, mtumiki wa munthu wa Mulungu kuti, "Tandiwuza zinthu zikuluzikulu zimene Elisa wachita."
[5] Pamene Gehazi ankayiwuza mfumuyo momwe Elisa anaukitsira anthu akufa, mayi amene mwana wake Elisa anamuukitsa kwa akufayo analowa kudzafunsa mfumu za nyumba yake ndi munda wake.
Gehazi anati, "Mbuye wanga mfumu, mayi wake ndi uyu ndipo mwana
wakeyo ndi uyu amene Elisa anamuukitsa kwa akufa." [6] Mfumu inafunsa
mayiyo za nkhaniyi ndipo iye anayifotokozera mfumuyo.
Ndipo mfumu inasankha munthu woti ayendetse nkhani yake ndipo inati, "Mubwezereni zonse zimene zinali zake, kuphatikizapo phindu lonse lochokera m'munda wake, kuyambira tsiku limene anachoka mpaka tsopano lino."

*Hazaeli Apha Beni-Hadadi*

[7] Elisa anapita ku Damasiko, ndipo Beni-Hadadi mfumu ya ku Aramu ankadwala. Mfumuyo itawuzidwa kuti, "Munthu wa Mulungu wabwera
kuno kuchokera kutali," [8] inawuza Hazaeli kuti, "Tenga mphatso ndipo pita ukakumane ndi munthu wa Mulungu. Ukandifunsire kwa Yehova kudzera mwa iye kuti, 'Kodi ndidzachira matenda angawa?' "
[9] Choncho Hazaeli anapita kukakumana ndi Elisa, atasenzetsa ngamira 40 mphatso za zinthu zosiyanasiyana zabwino kwambiri za ku Damasiko. Iye analowa m'nyumba ya Elisa ndi kuyima pamaso pake, ndipo anati, "Mwana wanu Beni-Hadadi wanditumа kuti ndidzakufunseni kuti, 'Kodi ndidzachira matenda angawa?' "

10 Elisa anayankha kuti, “Pita ndipo ukamuwuze kuti, ‘Udzachira
ndithu,’ koma Yehova wandionetsa kuti adzafabe.” 11 Elisa ana-
muyang’ana kwambiri Hazaeli mpaka anachita manyazi. Pamenepo
munthu wa Mulungu anayamba kulira.
12 Hazaeli anafunsa kuti, “Mbuye wanga mukulira chifukwa chiyani?”

Elisa anayankha kuti, “Chifukwa ndikudziwa choyipa chimene udzachi-
tira Aisraeli. Udzatentha mizinda yawo ya chitetezo, udzapha anyamata
awo ndi lupanga, udzaphwanyitsa pansi makanda awo ndiponso udza-
tumbula mimba za akazi awo oyembekezera.”
13 Ndipo Hazaeli anati, “Kodi kapolo wanune, amene ndine wonyozeka
ngati galu, ndingathe bwanji kuchita chinthu chachikulu chotere?”

Elisa anayankha kuti, “Yehova wandionetsa kuti iwe udzakhala mfumu
ya ku Aramu.”
14 Choncho Hazaeli anasiyana ndi Elisa ndi kubwerera kwa mbuye wake.
Beni-Hadadi atafunsa kuti, “Elisa wakuwuza chiyani?” Hazaeli anayankha
kuti, “Elisa wandiwuza kuti inu mudzachira ndithu.” 15 Koma mmawa
mwake Hazaeli anatenga nsalu yokhuthala ndi kuyiviyika m’madzi ndipo
anaphimba nayo nkhope ya mfumu, kotero mfumuyo inafa. Hazaeli
analowa ufumu m’malo mwake.

### *Yehoramu Mfumu ya ku Yuda*

16 Chaka chachisanu cha ufumu wa Yoramu mwana wa Ahabu mfumu
ya ku Israeli, Yehosafati ali mfumu ya ku Yuda, Yehoramu mwana wake
anakhala mfumu ya Ayuda. 17 Yehoramu analowa ufumu ali ndi zaka 32,
ndipo analamulira mu Yerusalemu zaka zisanu ndi zitatu. 18 Iye anatsatira
khalidwe la mafumu a ku Israeli, monga mmene linachitira banja la
Ahabu, popeza iye anakwatira mwana wa Ahabu. Yehoramu anachita
zoyipa pamaso pa Yehova. 19 Komabe, chifukwa cha mtumiki wake Davide,
Yehova sanafune kuwononga Yuda popeza Yehova analonjeza Davide kuti
adzamupatsa nyale pamodzi ndi zidzukulu zake mpaka muyaya.
20 Pa nthawi ya Yehoramu, Edomu anawukira ulamuliro wa Yuda
ndipo anadzisankhira mfumu. 21 Choncho Yehoramu anapita ku Zairi
pamodzi ndi magaleta ake onse. Ndipo iye anakantha Aedomu amene
anamuzungulira pamodzi ndi oyendetsa magaleta ake usiku. Koma
ankhondo ake anathawa napita ku misasa yawo. 22 Mpaka lero lino Edomu
ndi wowukira Yuda. Nthawi yomweyo mzinda wa Libina unawukiranso.
23 Ndipo ntchito zina za Yehoramu ndi zonse zomwe anachita, kodi
sizinalembedwe m’buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 24 Choncho
Yehoramu anamwalira ndipo anayikidwa m’manda pamodzi ndi makolo
ake mu Mzinda wa Davide. Ndipo Ahaziya mwana wake analowa ufumu
m’malo mwake.

### *Ahaziya Mfumu ya ku Yuda*

25 M’chaka cha khumi ndi chiwiri cha Yoramu mwana wa Ahabu mfumu
ya Israeli, Ahaziya mwana wa Yehoramu mfumu ya Yuda anayamba
kulamulira. 26 Ahaziya anali ndi zaka 22 pamene anakhala mfumu ndipo
analamulira mu Yerusalemu chaka chimodzi. Amayi ake anali Ataliya,
chidzukulu cha Omiri mfumu ya Israeli. 27 Iye anatsatira makhalidwe
a banja la Ahabu ndipo anachita zoyipa pamaso pa Yehova, monga
linachitira banja la Ahabu, pakuti anali mkamwini wa banja la Ahabu.
28 Ahaziya anapita pamodzi ndi Yoramu mwana wa Ahabu kukachita
nkhondo ndi Hazaeli mfumu ya Aramu ku Ramoti Giliyadi. Aaramu

anavulaza Yoramu. 29 Choncho mfumu Yoramu inabwerera ku Yezireeli
kuti ikachire mabala ake amene Aaramu anamuvulaza ku Rama pa
nkhondo yake ndi Hazaeli mfumu ya Aramu.

Tsono Ahaziya mwana wa Yehoramu mfumu ya ku Yuda anapita
ku Yezireeli kuti akamuone Yoramu mwana wa Ahabu, popeza n'kuti
akudwala.

# 9

### *Yehu Adzozedwa Ufumu wa ku Israeli*

1 Mneneri Elisa anayitanitsa mmodzi mwa ana a aneneri, namuwuza
kuti, "Manga lamba m'chiwuno mwako, tenga botolo la mafuta m'dzanja
lako ndipo upite ku Ramoti Giliyadi. 2 Ukakafika kumeneko, ukafunefune
Yehu mwana wa Yehosafati, mwana wa Nimisi. Ukapite kwa iye,
ukamuchotse pakati pa anzake ndi kukamulowetsa m'chipinda cham'kati.
3 Ndipo ukatenge botololi ndi kuthira mafuta pa mutu wake ndipo ukanene
kuti, 'Yehova akuti, Ine ndikudzoza iwe kukhala mfumu ya Israeli.'
Kenaka ukatsekule chitseko ndi kuthawa ndipo usakachedwe!"

4 Choncho mneneri wachinyamatayo anapita ku Ramoti Giliyadi.
5 Atafika ku Giliyadiko anapeza atsogoleri a ankhondo ali pa msonkhano.
Iye anati, "Mtsogoleri, ine ndili ndi uthenga wanu."

Ndipo Yehu anafunsa kuti, "Uthengawo ndi wa yani pakati pathu?"

Mneneriyo anayankha kuti, "Ndi wa inuyo, mtsogoleri."

6 Yehu anayimirira nakalowa m'nyumba. Pamenepo mneneriyo
anakhuthulira mafuta pamutu pa Yehu ndipo ananena kuti, "Yehova
Mulungu wa Israeli akuti, 'Ine ndikukudzoza kukhala mfumu ya Israeli,
anthu a Yehova. 7 Uyenera kuwononga nyumba ya mbuye wako Ahabu
ndipo ndidzabwezera imfa ya atumiki anga, aneneri ndiponso imfa ya
atumiki ena onse a Yehova amene anaphedwa ndi Yezebeli. 8 Banja
lonse la Ahabu lidzatheratu. Ndidzachotsa munthu aliyense wamwamuna
wa banja la Ahabu kaya ndi kapolo kapena mfulu. 9 Ndidzachititsa
kuti banja la Ahabu lifanane ndi banja la Yeroboamu mwana wa Nebati
ndiponso ngati banja la Baasa mwana wa Ahiya. 10 Kunena za Yezebeli,
agalu adzamudya ku dera la Yezireeli ndipo palibe amene adzamuyike
m'manda.' " Kenaka mneneriyo anatsekula chitseko n'kuthawa.

11 Yehu atatuluka kupita kumene kunali atsogoleri anzake, mmodzi mwa
iwo anamufunsa kuti, "Kodi zonse zili bwino? Kodi munthu wamisala uja
anabwera kudzatani kwa iwe?"

Yehu anayankha kuti, "Iwe ukumudziwa munthu uja ndiponso
ukudziwa zomwe amayankhula."

12 Atsogoleri aja anati, "Ukunama! Tiwuze."

Yehu anati, "Zimene wandiwuza ndi izi: 'Yehova akuti: Ine ndakudzoza
iwe kukhala mfumu ya Israeli.' "

13 Atsogoleri aja mofulumira anatenga zofunda zawo naziyala pansi pa
makwerero kuti Yehu akhalepo. Kenaka analiza lipenga, nafuwula kuti,
"Yehu ndiye mfumu!"

### *Yehu Apha Yoramu ndi Ahaziya*

14 Choncho Yehu mwana wa Yehosafati, mwana wa Nimisi, anachitira
chiwembu Yoramu. (Nthawi imeneyi n'kuti Yoramu ndi Aisraeli onse
akuteteza Ramoti Giliyadi kwa Hazaeli mfumu ya ku Aramu, 15 koma
n'kuti Yoramu atabwerera ku Yezireeli kuti akachire mabala amene

Aaramu anamuvulaza pa nkhondo ndi Hazaeli mfumu ya ku Aramu.)
Yehu anati, “Ngati mukugwirizana nazo zimenezi, wina aliyense asatuluke mu mzinda muno kupita kukafotokoza nkhaniyi ku Yezireeli.”
16 Pamenepo Yehu anakwera galeta lake, napita ku Yezireeli, chifukwa Yoramu anali akupumula kumeneko ndipo Ahaziya, mfumu ya ku Yuda, n’kuti ali komweko kudzamuona.

17 Mlonda amene ankayimirira pa nsanja yolondera mzinda wa Yezireeli ataona gulu lankhondo la Yehu likuyandikira, anafuwula kuti, “Ndikuona gulu lankhondo likubwera.”

Yoramu analamula kuti, “Peza munthu wokwera kavalo, mutume kuti akakumane nawo ndi kuwafunsa kuti, ‘Kodi mukubwera mwamtendere?’ ”

18 Choncho munthu wokwera kavalo anapita kukakumana ndi Yehu ndipo anati, “Mfumu ikufunsa kuti, ‘Kodi mukubwera mwamtendere?’ ”

Yehu anayankha kuti, “Kodi iwe nkhani ya mtendere yakukhudza bwanji? Tiye, zinditsata pambuyo panga.”

Mlonda uja anakafotokoza kwa mfumu kuti, “Wamthenga uja wakafika kwa anthuwo koma sakubwerera.”

19 Choncho mfumu inatumanso munthu wina wachiwiri wokwera kavalo. Atafika kwa anthuwo iye anati, “Mfumu ikufunsa kuti, ‘Kodi mukubwera mwamtendere?’ ”

Yehu anayankha kuti, “Kodi iwe nkhani ya mtendere yakukhudza bwanji? Tiye, zinditsata pambuyo panga.”

20 Mlonda uja anakanenanso kuti, “Wamthenga uja wakafika kwa anthuwo koma sakubwereranso. Kuyendako kukukhala ngati kwa Yehu mwana wa Nimisi, iye amayenda ngati munthu wamisala.”

21 Yoramu analamula kuti, “Konzani galeta langa.” Ndipo atakonza galeta lake, Yoramu mfumu ya Israeli ndi Ahaziya mfumu ya ku Yuda anakwera n’kutuluka mu mzindamo, aliyense atakwera galeta lake, kukakumana ndi Yehu. Iwo anakumana ndi Yehu pa munda umene unali
wa Naboti, wa ku Yezireeli. 22 Yoramu ataona Yehu anafunsa kuti, “Yehu,
kodi wabwera mwamtendere?”

Yehu anayankha kuti, “Pangakhale bwanji mtendere pamene zopembedza mafano zonse zilipo ndiponso ufiti wa amayi ako Yezebeli uli ponseponse?”

23 Yoramu anatembenuka, nathawa akufuwula kwa Ahaziya kuti, “Ahaziya, anthuwa atiwukira!”

24 Pamenepo Yehu anakoka uta wake ndipo analasa Yoramu kumsana pakati pa mapewa. Muviwo unakalasa mtima wake ndipo anagwa pansi
m’galeta lakelo. 25 Yehu anawuza Bidikara, mtsogoleri wa galeta lake
kuti, “Munyamule ndipo ukamuponye m’munda umene unali wa Naboti wa ku Yezireeli, chifukwa kumbukira mmene iwe ndi ine tinkayenda pambuyo pa Ahabu abambo ake, kuti Yehova ananeneratu za iye kuti,
26 ‘Zoonadi dzulo ndinaona magazi a Naboti ndi magazi a ana ake, akutero Yehova, ndipo Ine ndidzakubwezera ndithu choyipa chimenechi pa munda womwe uno, akutero Yehova.’ Tsono munyamule ndipo ukamuponye m’mundamo, potsatira zimene Yehova ananena.”

27 Ahaziya mfumu ya ku Yuda ataona zimene zinachitika, anathawira ku Beti Hagani. Yehu anamuthamangitsa, uku akufuwula kuti, “Mupheninso!” Iwo anamuvulaza ali m’galeta lakelo pa njira yopita ku Guri pafupi ndi Ibuleamu, koma iye anathawira ku Megido ndipo
anakafera kumeneko. 28 Antchito ake anamunyamulira m’galeta kupita

naye ku Yerusalemu ndipo anamuyika m'manda pamodzi ndi makolo ake
mu mzinda wa Davide. 29 (M'chaka cha khumi ndi chimodzi cha ufumu
wa Yoramu mwana wa Ahabu, Ahaziya anakhala mfumu ya ku Yuda).

### *Kuphedwa kwa Yezebeli*

30 Kenaka Yehu anapita ku Yezireeli. Yezebeli atamva zimene zinachi-
tika, anapaka zodzikometsera m'maso, naluka tsitsi lake, namasuzumira
pa zenera. 31 Pamene Yehu ankalowa pa chipata iye anafunsa kuti, "Kodi
wabwera mwamtendere, iwe Zimuri, munthu wopha mbuye wako?"
32 Yehu anakweza maso nayang'ana pa zenera, ndipo anafuwula kuti,
"Kodi ndani ali mbali yanga? Ndani?" Anthu ofulidwa awiri kapena atatu
anayang'ana Yehu pansipo. 33 Yehu anawawuza kuti, "Muponyeni pansi!"
Motero anamuponya pansi ndipo magazi ake ena anafalikira pa khoma
ndi pa akavalo pamene ankamupondaponda.
34 Yehu analowa m'nyumba yaufumu ndipo anadya ndi kumwa. Kenaka
iye anati, "Kamutoleni mkazi wotemberedwayo, ndipo kamuyikeni
m'manda, popeza ndi mwana wa mfumu." 35 Koma atapita kuti aka-
muyike m'manda, sanapeze kanthu kupatula chibade cha mutu wokha,
mapazi ake ndi manja ake. 36 Choncho iwo anabwerera kwa Yehu ndi
kukamufotokozera kuti, "Mawu amene Yehova anayankhula kudzera mwa
mtumiki wake Eliya wa ku Tisibe ndi awa: Pa munda wa ku Yezireeli agalu
adzadya mtembo wa Yezebeli. 37 Mtembo wa Yezebeli udzakhala ngati
zinyalala pa munda wa ku Yezireeli, kotero kuti palibe amene adzathe
kunena kuti, 'Uyu ndi Yezebeli.' "

## 10

### *Kuphedwa kwa Banja la Ahabu*

1 Tsono Ahabu anali ndi ana aamuna 70 a ku Samariya. Ndipo Yehu
analemba makalata nawatumiza ku Samariya kwa atsogoleri a mu mzinda
wa Yezireeli, kwa akuluakulu ndiponso kwa amene ankalera ana a Ahabu,
nati, 2 "Inu mukangolandira kalatayi, popeza ana a mbuye wanu ali ndi
inu ndiponso muli ndi magaleta ndi akavalo, mzinda wotetezedwa ndi
zida zankhondo, 3 sankhani mwana wa mbuye wanu amene ndi wooneka
bwino ndiponso woyenera, mulowetseni ufumu wa abambo ake. Kenaka
muchite nkhondo kuteteza nyumba ya mbuye wanu."
4 Koma anthuwo anachita mantha kwambiri ndipo anati, "Taonani,
mafumu awiri sanathe kulimbana naye, nanga ife tingathe bwanji?"
5 Choncho woyang'anira nyumba ya mfumu, bwanamkubwa wa
mzinda, akuluakulu ena ndiponso olera anawo anatumiza uthenga uwu
kwa Yehu: "Ife ndife atumiki anu ndipo tidzachita chilichonse chomwe
mutiwuze. Sitidzasankha munthu wina aliyense kukhala mfumu ndipo
chitani chimene mukuganiza kuti n'chabwino kwa inu."
6 Ndipo Yehu anawalembera kalata yachiwiri yonena kuti, "Ngati inu
muli mbali yanga ndi kuti mudzandimvera, mudule mitu ya ana a mbuye
wanu ndipo mubwere nayo kwa ine ku Yezireeli mawa nthawi ngati
yomwe ino."
Tsono ana a mfumu onse 70 anali pamodzi ndi akuluakulu a mu
mzindamo, amene ankawalera. 7 Kalatayo itafika, anthuwo anatenga ana
a mfumu 70 aja ndi kuwapha onse. Anayika mitu yawo m'madengu ndi
kuyitumiza ku Yezireeli kwa Yehu. 8 Mthenga uja atafika, anamuwuza
Yehu kuti, "Abweretsa mitu ya ana a mfumu."

Ndipo Yehu analamula kuti, “Unjikani mituyo m’milu iwiri pa chipata
cha mzinda ndipo ikhale pamenepo mpaka mmawa.”

9 Mmawa mwake Yehu anatuluka. Iye anayimirira pamaso pa anthu
onse ndipo anati, “Inu ndinu osalakwa. Ndine amene ndinachita
chiwembu mbuye wanu ndi kumupha, koma kodi wapha anthu onsewa
ndani? 10 Koma dziwani tsono, kuti mawu amene Yehova anayankhula
kunena za banja la Ahabu sadzapita padera. Yehova wachita chimene
analonjeza kudzera mwa mtumiki wake Eliya.” 11 Choncho Yehu anapha
onse amene anatsala a m’banja la Ahabu ku Yezireeli, pamodzinso ndi
akuluakulu ake onse, abwenzi ake ndiponso ansembe ake, sanasiyeko ndi
mmodzi yemwe wamoyo.

12 Kenaka Yehu ananyamuka kupita ku Samariya. Atafika pa malo
otchedwa Beti-Ekedi wa abusa, 13 Yehu anakumana ndi abale ena a
Ahaziya mfumu ya Yuda nawafunsa kuti, “Kodi ndinu yani?”

Iwo anayankha kuti, “Ndife abale ake a Ahaziya, ndipo tabwera
kulonjera banja la mfumu ndi ana a mfumukazi.”

14 Yehu analamula kuti, “Atengeni amoyo!” Choncho anawatenga amoyo
ndipo anakawaphera ku chitsime cha ku malo otchedwa Beti-Ekedi wa
abusa; anthu onse 42. Iye sanasiyepo ndi mmodzi yemwe wamoyo.

15 Yehu atachoka kumeneko anakumana ndi Yehonadabu mwana wa
Rekabu, amene amabwera kudzakumana naye. Yehu anamulonjera nati
kwa iye, “Kodi mtima wako uli bwino monga momwe mtima wanga
ugwirizana nawo mtima wako?”

Yehonadabu anayankha kuti, “Inde ndikugwirizana nawe.”

Yehu anati, “Ngati ndi choncho, gwire dzanja.” Ndipo iye anaterodi,
ndipo Yehu anamugwira dzanja namulowetsa m’galeta lake. 16 Yehu
anati, “Tiye kuno uwone mmene ndikudziperekera kwa Yehova.” Ndipo
anayenda naye m’galeta mwake.

17 Yehu atafika ku Samariya, anapha onse amene anatsala a m’banja la
Ahabu ku Samariya; anawawononongeratu potsata mawu a Yehova amene
anayankhula kudzera mwa Eliya.

### *Aneneri a Baala Aphedwa*

18 Ndipo Yehu anasonkhanitsa anthu onse pamodzi nawawuza kuti,
“Ahabu ankatumikira Baala pang’ono chabe; Yehu adzamutumikira
kwambiri. 19 Tsopano itanani aneneri a Baala onse, atumiki ake onse
ndi ansembe ake onse. Pasapezeke ndi mmodzi yemwe wotsala chifukwa
ine ndidzapereka nsembe yayikulu kwa Baala. Aliyense amene alephere
kubwera adzaphedwa.” Koma Yehu anachita zimenezi mwachinyengo ndi
cholinga choti awononge atumiki onse a Baala.

20 Yehu anati, “Itanitsani msonkhano wodzalemekeza Baala.” Ndipo
analengeza za msonkhanowo. 21 Pamenepo Yehu anatumiza mawu ku
dziko lonse la Israeli ndipo atumiki onse a Baala anabwera; palibe
ndi mmodzi yemwe amene anatsala. Iwo anadzaza nyumba ya Baala.
Nyumbayo inadzaziratu kuchokera ku khoma lina mpaka ku khoma lina.
22 Ndipo Yehu anawuza munthu wosunga mikanjo kuti, “Bweretsa mikanjo
yokwanira atumiki onse a Baala.” Ndipo iye anabweretsa mikanjoyo.

23 Kenaka Yehu ndi Yehonadabu mwana wa Rekabu analowa m’nyumba
ya Baala. Yehu anawawuza atumiki a Baala kuti, “Yang’anitsitsani ndipo
muone kuti muno musapezeke atumiki a Yehova, koma mukhale atumiki
okhawo a Baala.” 24 Choncho Yehu analowa kukapereka nsembe zina ndi
nsembe zopsereza. Nthawi iyi n’kuti Yehu atayika anthu 80 kunja kwa

nyumbayo ndi chenjezo lakuti, “Ngati wina aliyense wa inu adzathawitsa
wina aliyense wa anthu amene ndayika kuti muziwayang’anira, munthu
woteroyo adzaphedwa.”

25 Yehu atangotsiriza kupereka nsembe yopsereza, analamula alonda
ndi akulu a ankhondo kuti, “Lowani ndipo mukawaphe ndipo musalole
kuti wina athawe.” Choncho iwo anawapha ndi lupanga. Alonda ndi
akulu a ankhondo anaponya mitembo ya anthuwo panja ndipo anakalowa
m’kati mwenimweni mwa nyumba ya Baala. 26 Iwo anakatulutsa
mwala wopatulika umene unali m’nyumba ya Baala ndipo anawutentha.
27 Anawononga mwala wopatulika wa Baala ndi kugwetsa nyumba ya
Baala, ndipo anthu anayisandutsa chimbudzi mpaka lero lino.

28 Motero Yehu anawononga Baala mu Israeli. 29 Koma Yehuyo sanaleke
machimo a Yeroboamu mwana wa Nebati amene anachimwitsa nawo
Israeli kupembedza mafano a golide a ana ang’ombe ku Beteli ndi ku Dani.

30 Yehova anati kwa Yehu, “Chifukwa wachita bwino pokwaniritsa
kuchita zabwino pamaso panga ndipo wachitira banja la Ahabu zonse
zimene zinali m’maganizo anga, zidzukulu zako zidzakhala pa mpando
waufumu wa Israeli mpaka m’bado wachinayi.” 31 Komatu Yehu
sanasamalire kusunga lamulo la Yehova Mulungu wa Israeli ndi mtima
wake wonse. Iyeyo sanaleke machimo a Yeroboamu amene anachimwitsa
nawo Israeli.

32 Masiku amenewo Yehova anayamba kuchepetsa dziko la Israeli.
Hazaeli anagonjetsa Aisraeli, 33 kuyambira kummawa kwa Yorodani, dziko
lonse la Giliyadi (chigawo cha Gadi, Rubeni ndi Manase), kuchokera ku
Aroeri pafupi ndi chigwa cha Arinoni kudutsa Giliyadi mpaka ku Basani.

34 Ntchito zina za Yehu ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalembedwe
m’buku la mbiri ya mafumu a ku Israeli?

35 Yehu anamwalira ndipo anayikidwa m’manda pamodzi ndi makolo
ake ku Samariya. Ndipo Yehowahazi mwana wake analowa ufumu
m’malo mwake. 36 Yehu analamulira Aisraeli ku Samariya zaka 28.

# 11

### *Ataliya ndi Yowasi*

1 Ataliya amayi ake a Ahaziya ataona kuti mwana wawo wafa, ananya-
muka nakawononga banja lonse la mfumu. 2 Koma Yehoseba, mwana
wamkazi wa Mfumu Yehoramu, mlongo wake wa Ahaziya, anatenga
Yowasi mwana wa Ahaziya, namusunga kutali ndi ana a mfumu amene
ankati awaphewo. Anamuyika iye pamodzi ndi mlezi wake m’chipinda
chogona cham’kati kubisira Ataliya kotero iye sanaphedwe. 3 Mwanayo
anakhala mobisala pamodzi ndi mlezi wake m’nyumba ya Yehova kwa
zaka zisanu ndi chimodzi pamene Ataliya ankalamulira dzikolo.

4 Koma m’chaka chachisanu ndi chiwiri, Yehoyada anatumiza mawu
kukayitana atsogoleri olamulira asilikali 100 olondera mfumu ndiponso
alonda olonda nyumba yaufumu ndipo anabwera nawo m’Nyumba
ya Yehova. Iye anapangana nawo pangano ndipo anawalumbiritsa
m’nyumba ya Yehova. Kenaka anawaonetsa mwana wamwamuna wa
mfumu uja. 5 Yehoyada anawalamulira kuti, “Chimene muti muchite ndi
ichi: Inu magulu atatu amene muti mudzakhale pa ntchito tsiku la Sabata,
gulu loyamba lidzalondera nyumba ya mfumu, 6 gulu lachiwiri lidza-
londera Chipata cha Suri, ndipo gulu lachitatu lidzalondera chipata cha
kumbuyo kwa asilikali amene amasinthana polondera nyumbayo. 7 Ndipo

inu amene muli m'magulu ena awiri amene simugwira ntchito pa tsiku la
Sabata, nonse mudzalondere mfumu ku nyumbayo. 8 Mudzakhale mozun-
gulira mfumuyo, munthu aliyense ali ndi chida m'manja mwake. Wina
aliyense amene adzakuyandikireni adzayenera kuphedwa. Muzikhala
pafupi ndi mfumu kulikonse kumene ikupita."
9 Atsogoleri olamulira asilikali 100 aja anachitadi zonse monga anala-
mulira wansembe Yehoyada. Aliyense anatenga anthu ake, iwo amene
amakagwira ntchito pa tsiku la Sabata ndi amene amapita kukapuma
ndipo anabwera kwa wansembe Yehoyada. 10 Ndipo wansembeyo
anawapatsa asilikaliwo mikondo ndi zishango zimene zinali za mfumu
Davide ndipo zinali m'Nyumba ya Yehova. 11 Alondawo, aliyense ali ndi
chida m'manja mwake, anayima mozungulira mfumu, pafupi ndi guwa
lansembe ndi nyumbayo, kuchokera mbali ya kummwera mpaka mbali
ya kumpoto kwa nyumbayo.
12 Yehoyada anatulutsa mwana wa mfumuyo namuveka chipewa chau-
fumu ndipo anamupatsa Buku la Chipangano ndi kumuyika kukhala
mfumu. Iwo anamudzoza ndipo anthu anamuwombera m'manja aku-
fuwula kuti, "Mfumu ikhale ndi moyo wautali!"
13 Ataliya atamva phokoso limene alonda ndi anthuwo amachita, anapita
ku Nyumba ya Yehova kumene kunali anthuwo. 14 Iye anayang'ana naona
mfumu itayima pa chipilala, potsata mwambo waufumu. Atsogoleri a
asilikali ndi oyimba malipenga anali pafupi ndi mfumuyo, ndipo anthu
onse a m'deralo ankasangalala ndi kuyimba malipenga. Pamenepo Ataliya
anang'amba mkanjo wake nafuwula kuti, "Kuwukira! Kuwukira!"
15 Wansembe Yehoyada analamula atsogoleri a asilikali 100 amene
amayang'anira asilikaliwo kuti, "Mutulutseni ameneyo pakati panu ndipo
muphe ndi lupanga aliyense amene adzamutsata." Pakuti n'kuti wansem-
beyo atanena kuti, "Ataliyayo asaphedwere m'Nyumba ya Yehova."
16 Choncho anamugwira pamene amafika pa malo amene akavalo amalow-
era ku nyumba ya mfumu ndipo anamuphera pamenepo.
17 Tsono Yehoyada anachititsa pangano pakati pa Yehova ndi mfumu ndi
anthu kuti adzakhala anthu a Yehova. Iye anachititsanso pangano pakati
pa mfumu ndi anthu. 18 Anthu onse a m'dzikomo anapita ku nyumba
ya Baala nakayigwetsa. Iwo anaphwanya kotheratu maguwa ansembe
ndi mafano ake ndipo anapha Matani wansembe wa Baala patsogolo pa
maguwa pomwepo.
Pamenepo wansembe Yehoyada anasankha oyang'anira Nyumba ya
Yehova. 19 Iye anatenga atsogoleri a asilikali 100 aja, alonda olonda
nyumba yaufumu pamodzi ndi anthu onse a m'dzikomo ndipo onse
pamodzi anayitulutsa mfumu m'Nyumba ya Yehova ndi kukalowa ku
nyumba yaufumu podzera pa chipata cha alonda. Ndipo mfumuyo
inakhala pa mpando wake waufumu. 20 Choncho anthu onse a m'dzikomo
anasangalala. Ndipo mu mzindamo munakhala bata chifukwa Ataliya
n'kuti ataphedwa ndi lupanga ku nyumba ya mfumu.
21 Yowasi anali wa zaka zisanu ndi ziwiri pamene anayamba kulamulira.

# 12

*Yowasi Akonzanso Nyumba ya Yehova*

1 M'chaka chachisanu ndi chiwiri cha Yehu, Yowasi anakhala mfumu,
ndipo analamulira mu Yerusalemu zaka makumi anayi. Amayi ake anali

Zibiya wa ku Beeriseba. [2] Yowasi anachita zolungama pamaso pa Yehova
masiku onse amene wansembe Yehoyada ankamulangiza. [3] Komabe sana-
chotse malo opembedzerapo mafano ndipo anthu anapitiriza kupereka
nsembe ndi kufukiza lubani ku malo opembedzerako mafanowo.

[4] Yowasi anati kwa ansembe, "Tolerani ndalama zonse zimene
zimaperekedwa monga chopereka chopatulika ku Nyumba ya Yehova,
ndalama zonse zamsonkho wa munthu aliyense, ndalama zomwe munthu
amapereka akalonjeza ndiponso ndalama zimene munthu amapereka
mwaufulu ku Nyumba ya Yehova. [5] Wansembe aliyense alandire ndala-
mazo kuchokera kwa abwenzi ake, ndipo zigwiritsidwe ntchito yokonzera
chilichonse chimene chipezeke kuti ndi chowonongeka m'nyumbayo."

[6] Koma pofika chaka cha 23 cha ufumu wa Yowasi, ansembewo anali
asanakonze nyumbayo. [7] Choncho Mfumu Yowasi inayitanitsa wansembe
Yehoyada ndi ansembe ena ndipo inafunsa kuti, "Chifukwa chiyani
simukukonza malo owonongeka a m'nyumbayi? Musasungenso ndalama
zina zochokera kwa abwenzi anu, koma muzipereke kuti akonzere
nyumbayi." [8] Ansembe anavomera kuti salandiranso ndalama kuchokera
kwa anthu ndipo kuti sindiwo amene ati akonzenso nyumbayo.

[9] Koma wansembe Yehoyada anatenga bokosi ndipo anabowola
chivundikiro chake. Anayika bokosilo pambali pa guwa lansembe,
kudzanja lamanja la aliyense amene akulowa m'Nyumba ya Yehovayo.
Ansembe amene ankalondera pa khomopo ankaponya m'bokosi ndalama
zonse zimene ankabwera nazo ku nyumba ya Yehova. [10] Nthawi zonse
akaona kuti m'bokosimo muli ndalama zambiri, mlembi wa mfumu ndi
mkulu wa ansembe ankabwera ndipo ankawerenga ndalama zomwe
anthu ankabwera nazo ku Nyumba ya Yehova ndi kuziyika m'matumba.
[11] Ankati akadziwa kuti ndalamazo zilipo zingati, ankazipereka kwa anthu
amene ankayang'anira ntchito yokonza nyumbayo. Ndalamazo ankalipira
anthu amene ankagwira ntchito yokonza Nyumba ya Yehova, amisiri a
matabwa ndi amisiri omanga nyumba, [12] amisiri a miyala ndiponso anthu
ophwanya miyala. Iwo ankagula matabwa ndi miyala yosema yokonzera
Nyumba ya Yehova ndipo ankalipira zinthu zonse zofunika pokonzanso
nyumbayo.

[13] Koma ndalama zomwe anthu ankabwera nazo ku nyumbayo sanag-
ulire siliva wopangira mabeseni, zozimitsira nyale, mbale zowazira mag-
azi, malipenga kapena ziwiya zina zilizonse zagolide kapena zasiliva za ku
Nyumba ya Yehova. [14] Ndalamazi anazipereka kwa anthu antchito amene
anazigwiritsa ntchito yokonzera nyumbayo. [15] Koma sanawafunse kuti
afotokoze kagwiritsidwe ntchito ka ndalama zolipira amene ankagwira
ntchito, chifukwa anthuwo ankagwira ntchitoyo mokhulupirika kwambiri.
[16] Ndalama zomwe zinkaperekedwa pa nsembe yopepesera machimo ndi
nsembe yoperekedwa chifukwa cha tchimo sanabwere nazo ku Nyumba
ya Yehova pakuti zinali za ansembe.

[17] Pa nthawi imeneyo, Hazaeli, mfumu ya Aramu anapita kukathira
nkhondo mzinda wa Gati nawulanda. Kenaka Hazaeli anatembenuka
kupita kukathira nkhondo mzinda wa Yerusalemu. [18] Koma Yowasi
mfumu ya Yuda anatenga zinthu zonse zopatulika zomwe anazipatula
Yehosafati, Yehoramu, ndi Ahaziya abambo ake, mafumu a Yuda ndi
mphatso zonse zomwe iye mwini anazipereka: golide yense amene
anapezeka m'nyumba yosungiramo chuma cha m'nyumba ya Yehova ndi

zomwe zinali m'nyumba ya mfumu, nazipereka kwa Hazaeli mfumu ya
Aramu. Pamenepo iye anachoka ku Yerusalemuko.

19 Ndipo ntchito zina za Yowasi ndi zonse zimene anachita, kodi
sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 20 Akuluakulu ake
anamuchitira chiwembu ndi kumupha ku Beti Milo, pa njira yotsikira ku
Silo. 21 Yozakara mwana wa Simeati ndi Yehozabadi mwana wa Someri
atumiki ake anamukantha nafa. Ndipo anamuyika m'manda pamodzi ndi
makolo ake mu Mzinda wa Davide. Ndipo Amaziya mwana wake analowa
ufumu m'malo mwake.

# 13

*Yehowahazi Mfumu ya Israeli*

1 M'chaka cha 23 cha ufumu wa Yowasi mwana wa Ahaziya mfumu
ya Yuda, Yehowahazi, mwana wa Yehu anakhala mfumu ya Israeli mu
Samariya, ndipo analamulira zaka 17. 2 Iye anachita zoyipa pamaso
pa Yehova potsatira machimo a Yeroboamu mwana Nebati amene
anachimwitsa nawo Israeli ndipo iye sanawaleke machimowo. 3 Ndipo
Yehova anakwiyira Aisraeli nawayika pansi pa ulamuliro wa Hazaeli
mfumu ya Siriya ndi Beni-Hadadi mwana wa Hazaeli masiku awo onse.

4 Tsono Yehowahazi anapempha Yehova kuti amuchitire chifundo ndipo
Yehova anamva pempho lake chifukwa anaona momwe mfumu ya
Aramu inkapsinjira Aisraeli. 5 Yehova anapatsa Aisraeli munthu woti
awapulumutse ndipo anapulumuka m'dzanja la Aramu. Choncho Aisraeli
anakhala m'nyumba zawo monga ankachitira kale. 6 Komabe Aisraeli
sanaleke kuchita machimo a nyumba ya Yeroboamu, amene anachimwitsa
nawo Israeli. Iwo anapitirira kuchita machimowo. Ndiponso fano la Asera
linakhalabe ku Samariya.

7 Yehowahazi sanatsale ndi ankhondo ambiri koma 50 okha okwera pa
akavalo, magaleta khumi ndi asilikali oyenda pansi 10,000.

8 Ntchito zina za Yehowahazi ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli? 9 Yehowahazi anamwalira
ndipo anayikidwa m'manda mu Samariya. Ndipo Yowasi mwana wake
analowa ufumu m'malo mwake.

*Yehowasi Mfumu ya Israeli*

10 M'chaka cha 37 cha Yowasi mfumu ya Yuda, Yehowahazi anakhala
mfumu ya Israeli mu Samariya, ndipo analamulira zaka 16. 11 Iye anachita
zoyipa pamaso pa Yehova ndipo sanaleke kuchita tchimo la Yeroboamu
mwana wa Nebati limene anachimwitsa nalo Israeli.

12 Ntchito zina za Yowasi ndi zonse zimene anachita, kuphatikizapo
nkhondo yake ndi Amaziya mfumu ya Yuda, kodi sizinalembedwe m'buku
la mbiri ya mafumu a Israeli? 13 Yowasi anayikidwa m'manda pamodzi
ndi makolo ake ndipo Yeroboamu mwana wake analowa ufumu m'malo
mwake. Yowasi anayikidwa m'manda mu Samariya pamodzi ndi mafumu
a Israeli.

14 Tsono Elisa anadwala matenda amene anafa nawo. Yowasi mfumu ya
Israeli inapita kukamuona ndipo inamulirira. Iye polira ankanena kuti,
"Abambo anga! Abambo anga! Magaleta a Israeli ndi okwerapo ake a
Israeli!"

15 Elisa anamuwuza kuti, “Tenga uta ndi mivi.” Ndipo anaterodi. 16 Elisa
anawuza mfumu ya Israeli kuti, “Tenga uta m’dzanja lako.” Pamene
anatenga utawo, Elisa anayika manja ake pa manja a mfumuyo.

17 Elisa anamuwuza kuti, “Tsekula zenera.” Ndipo anatsekuladi. Elisa
anati, “Ponya muviwo!” Ndipo anaponyadi. Elisa anati, “Muvi wa
chigonjetso cha Yehova, muvi wogonjetsera Aaramu! Iwe udzawa-
wononga kwathunthu Aaramu ku Afeki.”

18 Kenaka Elisa anati, “Tenga mivi.” Ndipo mfumu inatenga
miviyo. Iye anati, “Lasa pansi.” Mfumu inalasa pansi miviyo katatu
n’kuleka. 19 Munthu wa Mulungu anapsera mtima mfumuyo ndipo anati,
“Ukanalasa pansi kasanu kapena kasanu n’kamodzi. Pamenepo ukanatha
kuwagonjetsa Aaramu ndi kuwawononga kwathunthu. Koma tsopano
udzawagonjetsa katatu kokha.”

20 Elisa anamwalira ndipo anayikidwa m’manda.

Tsono magulu a ankhondo a Amowabu ankabwera kudzalowa ndi
kudzathira nkhondo dzikolo nthawi ya dzinja. 21 Tsiku lina Aisraeli
ena akukayika maliro m’manda, mwadzidzidzi anaona gulu lankhondo
ndipo munthu womwalirayo anamuponyera m’manda a Elisa. Pamene
mtembowo unakhudza mafupa a Elisa, munthu wakufayo anatsitsimuka
nayimirira.

22 Hazaeli mfumu ya Aramu inazunza Aisraeli nthawi yonse ya ula-
muliro wa Yehowahazi. 23 Koma Yehova anawachitira chifundo Aisraeliwo
ndi kukhudzika ndi zomwe zinkawachitikira chifukwa cha pangano
lake ndi Abrahamu, Isake ndi Yakobo. Mpaka lero lino Iye sanafune
kuwawononga kapena kuwachotsa pamaso pake.

24 Hazaeli mfumu ya Aramu inamwalira ndipo mwana wake Beni-
Hadadi analowa ufumu m’malo mwake. 25 Pamenepo Yowasi mwana wa
Yehowahazi analandanso kwa Beni-Hadadi mwana wa Hazaeli mizinda
yonse imene iye analanda Yehowahazi abambo ake. Yehowasi anagonjetsa
Beni-Hadadi katatu ndipo anatenganso mizinda ya Israeli.

# 14

### *Amaziya Mfumu ya Yuda*

1 M’chaka chachiwiri cha Yehowasi mwana wa Yowahazi mfumu ya
Israeli, Amaziya mwana wa Yowasi mfumu ya Yuda anayamba kulamulira.
2 Iye anali ndi zaka 25 pamene anakhala mfumu ndipo analamulira mu
Yerusalemu zaka 29. Amayi ake anali Yehoyadini wa ku Yerusalemu.
3 Iye anachita zolungama pamaso pa Yehova, koma osafanana ndi zomwe
anachita Davide kholo lake. Iye anatsatira zochita zonse za Yowasi
abambo ake. 4 Komabe sanachotse malo opembedzerapo mafano. Anthu
anapitiriza kupereka nsembe ndi kufukiza lubani kumeneko.

5 Atakhazikika mu ufumu wake, Amaziya anapha atumiki ake amene
anapha abambo ake, mfumu ija. 6 Komatu iye sanaphe ana a anthu amene
anapha abambo ake potsatira zomwe zinalembedwa m’buku la Malamulo
a Mose. M’menemo Yehova analamula kuti, “Makolo asaphedwe chifukwa
cha ana awo, ndipo ana asaphedwe chifukwa cha makolo awo, koma
aliyense ayenera kufa chifukwa cha zolakwa zake.”

7 Iye ndiye amene anapha Aedomu 10,000 m’chigwa cha Mchere nalanda
mzinda wa Sela pa nkhondo ndipo anawutcha Yokiteeli, dzina lake ndi
lomwelo mpaka lero lino.

8 Tsono Amaziya anatuma amithenga kwa Yehowasi mwana wa Yehowa-
hazi, mwana wa Yehu mfumu ya Israeli ndi kumuopseza kuti, “Bwera
tidzaonane maso ndi maso.”
9 Koma Yehowasi mfumu ya Israeli anabweza mawu kwa Amaziya
mfumu ya Yuda kuti, “Mtengo wa minga wa ku Lebanoni unatumiza
uthenga kwa mkungudza wa ku Lebanoni. ‘Patse mwana wako wamkazi
kuti ndimukwatire.’ Kenaka chirombo cha ku Lebanoni chinabwera ndi
kupondaponda mtengo wa mingawo. 10 Inde iwe wagonjetsa Edomu ndipo
tsopano wayamba kudzikuza. Dzitamandire chifukwa cha kupambana
kwako, koma khala kwanu konko! N’chifukwa chiyani ukuyamba dala
mavuto amene adzakuwononga pamodzi ndi Yuda?”
11 Koma Amaziya sanamvere zimenezi. Choncho Yehowasi mfumu
ya Israeli anakamuthira nkhondo. Yehowasi ndi Amaziya anakumana
maso ndi maso ku Beti-Semesi m’dziko la Yuda. 12 Israeli anagonjetsa
Yuda ndipo munthu aliyense anathawira kwawo. 13 Yehowasi mfumu ya
Israeli anagwira Amaziya mfumu ya Yuda, mwana wa Yowasi, mwana wa
Ahaziya ku Beti-Semesi. Ndipo anapita ku Yerusalemu nakagwetsa khoma
la Yerusalemu kuyambira ku Chipata cha Efereimu mpaka ku Chipata
Chapangodya, gawo lotalika mamita 180. 14 Iye anatenga golide ndi siliva
yense pamodzi ndi ziwiya zonse zimene zinali m’Nyumba ya Yehova ndi
zimene zinali mosungira chuma cha nyumba ya mfumu. Iye anagwiranso
anthu nabwerera ku Samariya.
15 Ntchito zina za Yehowasi ndi zonse zimene anachita, kuwonjezera za
nkhondo yake ndi Amaziya mfumu ya Yuda, kodi sizinalembedwe m’buku
la mbiri ya mafumu a Israeli? 16 Yehowasi anamwalira ndipo anayikidwa
m’manda mu Samariya pamodzi ndi mafumu a Israeli. Ndipo mwana
wake Yeroboamu analowa ufumu m’malo mwake.
17 Amaziya mwana wa Yowasi mfumu ya Yuda anakhala zaka khumi ndi
zisanu atamwalira Yehowasi mwana wa Yehowahazi mfumu ya Israeli.
18 Ntchito zina za Amaziya, kodi sizinalembedwe m’buku la mbiri ya
mafumu a Yuda?
19 Anthu anapangana zomuchita chiwembu mu Yerusalemu ndipo
Amaziya anathawira ku Lakisi, koma anatumiza anthu ku Lakisiko
nakamuphera komweko. 20 Anabwera naye ku pa kavalo ku Yerusalemu
ndi kumuyika m’manda pamodzi ndi makolo ake mu Mzinda wa Davide.
21 Ndipo anthu onse a ku Yuda anatenga Azariya, amene anali ndi zaka
16 namulonga ufumu m’malo mwa abambo ake Amaziya. 22 Azariya
anamanga mzinda wa Elati ndi kuwubwezeretsa ku Yuda, Amaziya
atamwalira.

### *Mfumu Yeroboamu Wachiwiri wa ku Israeli*

23 M’chaka cha khumi ndi chisanu cha Amaziya mwana wa Yowasi
mfumu ya Yuda, Yeroboamu mwana wa Yehowasi mfumu ya Israeli
analowa ufumu ku Samariya ndipo analamulira za 41. 24 Iye anachita
zoyipa pamaso pa Yehova ndipo sanasiye machimo a Yeroboamu mwana
wa Nebati, amene anachimwitsa nawo Israeli. 25 Iye ndi amene anabwez-
eretsanso malire a Israeli kuyambira ku Lebo Hamati mpaka ku Nyanja
ya Araba, molingana ndi zimene ananena Yehova Mulungu wa Israeli,
kudzera mwa mtumiki wake Yona mwana wa Amitai, mneneri wochokera
ku Gati-Heferi.
26 Pakuti Yehova anaona masautso a Israeli amene anali owawa
kwambiri, panalibe kapolo kapena mfulu ngakhale wina aliyense amene

akanathandiza Israeli. [27] Pakuti Yehova anali asananene zofafaniza ufumu
wa Israeli pa dziko lapansi, Iye anawapulumutsa kudzera m'dzanja la
Yeroboamu mwana wa Yowasi.
[28] Ntchito zina za Yeroboamu ndi zonse zimene anachita, za kupambana
kwake pa nkhondo, za mmene anagonjetsera Damasiko ndi Hamati, imene
inali mizinda ya Yuda, kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu
a Israeli? [29] Yeroboamu anamwalira ndipo anayikidwa m'manda pamodzi
ndi mafumu a Israeli. Ndipo Zekariya mwana wake analowa ufumu
m'malo mwake.

# 15

*Azariya Mfumu ya Yuda*

[1] M'chaka cha 27 cha Yeroboamu mfumu ya Israeli, Azariya mwana wa
Amaziya mfumu ya Yuda anayamba kulamulira. [2] Iye anakhala mfumu
ali ndi zaka 16 ndipo analamulira mu Yerusalemu zaka 52. Amayi ake
anali Yekoliya wa ku Yerusalemu. [3] Iyeyo anachita zabwino pamaso
pa Yehova, monga momwe anachitira Amaziya abambo ake. [4] Komabe
malo opembedzerako mafano sanawachotse ndipo anthu anapitirizabe
kupereka nsembe ndi kufukiza lubani kumeneko.
[5] Ndipo Yehova analanga mfumu ndi nthenda ya khate mpaka tsiku
limene inamwalira. Tsono mfumuyo inkakhala m'nyumba yakeyake
yapadera. Mwana wake Yotamu ndiye amene ankayang'anira nyumba
ya mfumu ndiponso ndiye amene ankalamulira anthu m'dzikomo.
[6] Ntchito zina za Azariya ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? [7] Azariya anamwalira ndipo
anayikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake mu Mzinda wa Davide.
Ndipo Yotamu mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

*Zekariya Mfumu ya Israeli*

[8] M'chaka cha 38 cha Azariya mfumu ya Yuda, Zekariya mwana wa
Yeroboamu anakhala mfumu ya Israeli ku Samariya ndipo analamulira
miyezi isanu ndi umodzi. [9] Ndipo iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova
monga anachitira makolo ake. Iye sanaleke machimo a Yeroboamu
mwana wa Nebati, amene anachimwitsa nawo Israeli.
[10] Salumu mwana wa Yabesi anachitira chiwembu Zekariya. Anamukan-
tha anthu akuona, namupha, ndipo analowa ufumu m'malo mwake.
[11] Ntchito zina za Zekariya, zinalembedwa m'buku la mbiri ya mafumu
a Israeli. [12] Awa ndiwo mawu a Yehova amene anayankhula kwa Yehu
kuti, "Ana ako adzalamulira Israeli mpaka m'bado wachinayi."

*Salumu Mfumu ya Israeli*

[13] Salumu mwana wa Yabesi anakhala mfumu m'chaka cha 39 cha
ulamuliro wa Uziya mfumu ya Yuda ndipo analamulira mu Samariya
mwezi umodzi. [14] Ndipo Menahemu mwana wa Gadi anachoka ku Tiriza
napita ku Samariya nakantha Salumu mwana wa Yabesi ku Samariya,
namupha ndipo iye analowa ufumu m'malo mwake.
[15] Ntchito zina za Salumu ndiponso za chiwembu chimene anachita,
zinalembedwa m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli.
[16] Nthawi imeneyo Menahemu, kuchokera ku Tiriza, anakathira
nkhondo mzinda wa Tipisa ndi anthu onse amene anali m'menemo ndi
dera lonse lozungulira chifukwa iwo anakana kutsekula zipata zawo. Iye

anatenga katundu yense mu mzinda wa Tipisa ndi kutumbula akazi onse oyembekezera.

### *Menahemu Mfumu ya Israeli*

17 M'chaka cha 39 cha Azariya mfumu ya Yuda, Menahemu mwana wa Gadi anakhala mfumu ya Israeli ndipo analamulira mu Samariya
zaka khumi. 18 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova. Nthawi yonse ya ulamuliro wake sanasiye machimo a Yeroboamu mwana wa Nebati, amene anachimwitsa nawo Israeli.
19 Tsono Puli mfumu ya ku Asiriya inadzathira nkhondo dzikolo ndipo Menahemu anapatsa Puliyo makilogalamu 34,000 a siliva kuti
amuthandize ndi kulimbikitsa ufumu wake. 20 Menahemu anapeza ndalamazo kudzera mu msonkho umene ankakhometsa Aisraeli. Munthu aliyense wachuma ankapereka masekeli a siliva makumi asanu kwa mfumu ya ku Asiriya. Choncho mfumu ya ku Asiriya inabwerera ndipo sinakhalenso m'dzikomo.
21 Ntchito zina za Menahemu ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli? 22 Menahemu anamwalira ndipo anayikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake. Ndipo Pekahiya mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

### *Pekahiya Mfumu ya Israeli*

23 M'chaka cha makumi asanu a Azariya mfumu ya Yuda, Pekahiya mwana wa Menahemu anakhala mfumu ya Israeli mu Samariya ndipo
analamulira zaka ziwiri. 24 Pekahiya anachita zoyipa pamaso pa Yehova. Iye sanaleke machimo a Yeroboamu mwana wa Nebati, omwe
anachimwitsa nawo Israeli. 25 Ndipo Peka mwana wa Remaliya, mtsogoleri wake wa ankhondo, anamuchita chiwembu. Iye pamodzi ndi anthu makumi asanu a ku Giliyadi anapha Pekahiya pamodzi ndi Arigobu ndi Ariyeli m'chipinda choteteza nyumba ya mfumu mu Samariya. Kotero Peka anapha Pekahiya ndipo analowa ufumu m'malo mwake.
26 Ntchito zina za Pekahiya ndi zonse zimene anachita zinalembedwa m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli.

### *Peka Mfumu ya Israeli*

27 M'chaka cha 52 cha Azariya mfumu ya Yuda, Peka mwana wa Remaliya anakhala mfumu ya Israeli ku Samariya ndipo analamulira
zaka makumi awiri. 28 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova. Sanaleke machimo a Yeroboamu mwana wa Nebati, amene anachimwitsa nawo Israeli.
29 Nthawi ya Peka mfumu ya Israeli, Tigilati-Pileseri mfumu ya ku Asiriya anabwera ndi kudzalanda Iyoni, Abeli-Beti-Maaka, Yanowa, Kedesi ndi Hazori. Mfumu ya ku Asiriya inatenga Giliyadi ndi Galileya, kuphatikizanso madera onse a Nafutali ndipo anatumiza Aisraeli ku
Asiriya. 30 Kenaka Hoseya mwana wa Ela anachitira chiwembu Peka mwana wa Remaliya. Anamukantha ndi kumupha ndipo anakhala mfumu m'malo mwake m'chaka makumi awiri cha Yotamu mwana wa Uziya.
31 Ntchito zina za Peka ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli?

### *Yotamu Mfumu ya Yuda*

32 M'chaka chachiwiri cha Peka mwana wa Remaliya mfumu ya Israeli,
Yotamu mwana wa Uziya mfumu ya Yuda anayamba kulamulira. 33 Iye

anakhala mfumu ali ndi zaka 25 ndipo analamulira mu Yerusalemu zaka
16. Amayi ake anali Yerusa mwana wa Zadoki. 34 Iye anachita zabwino
pamaso pa Yehova monga anachitira Uziya abambo ake. 35 Komabe malo
opembedzera mafano sanawachotse ndipo anthu anapitiriza kupereka
nsembe ndi kufukiza lubani kumeneko.
36 Ntchito zina za Yotamu ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 37 (Nthawi imeneyo,
Yehova anayamba kumatuma Rezini mfumu ya Aaramu ndi Peka mwana
wa Remaliya kudzamenyana ndi Yuda). 38 Yotamu anamwalira ndipo
anayikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake mu Mzinda wa Davide
abambo ake. Ndipo Ahazi mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

# 16

*Ahazi Mfumu ya Yuda*

1 M'chaka cha 17 cha Peka mwana wa Remaliya, Ahazi mwana wa
Yotamu mfumu ya Yuda anayamba kulamulira. 2 Ahazi anakhala mfumu
ali ndi zaka makumi awiri ndipo analamulira mu Yerusalemu zaka 16.
Iye sanachite zabwino pamaso pa Yehova Mulungu wake monga momwe
Davide kholo lake ankachitira. 3 Iye anayenda m'njira ya mafumu
a Israeli mpaka kupereka mwana wake wamwamuna pa moto ngati
nsembe yopsereza, potsatira zonyansa za anthu a mitundu imene Yehova
anayipirikitsa m'dzikomo Aisraeli asanafike. 4 Iyeyo ankapereka nsembe
ndi kufukiza lubani pa malo opembedzera mafano, pa mapiri ndi pansi
pa mtengo uliwonse wa masamba ambiri.
5 Ndipo Rezini mfumu ya Aramu ndi Peka mwana wa Remaliya mfumu
ya Israeli anapita kukachita naye nkhondo ku Yerusalemu ndipo anazinga
Ahazi, koma sanathe kumugonjetsa. 6 Nthawi imeneyo Rezini mfumu ya
Aramu anatenganso Elati ndi kumubwezera kwa Aaramu, nathamangitsa
anthu a ku Yuda mu Elatimo. Aedomu anapita kukakhala ku Elati ndipo
akukhalako mpaka lero lino.
7 Ahazi anatuma amithenga kwa Tigilati-Pileseri mfumu ya ku Asiriya
kuti, "Ine ndine mtumiki wanu ndipo ndili pansi panu. Bwerani
mudzandipulumutse m'dzanja la mfumu ya Aramu ndiponso m'dzanja la
mfumu ya Israeli amene akundithira nkhondo." 8 Ndipo Ahazi anatenga
siliva ndi golide amene anamupeza m'Nyumba ya Yehova ndi mosungira
chuma cha nyumba ya mfumu ndi kutumiza ngati mphatso kwa mfumu ya
ku Asiriya. 9 Mfumu ya ku Asiriya inamvera pokathira nkhondo mzinda
wa Damasiko ndi kuwulanda. Anthu a mu mzindamo anawatumiza ku
Kiri ndipo anapha Rezini.
10 Kenaka mfumu Ahazi inapita ku Damasiko kukakumana ndi Tigilati-
Pileseri mfumu ya ku Asiriya. Iye anaona guwa lansembe ku Damasiko
kuja ndipo anatumiza chitsanzo chake kwa wansembe Uriya, osasiyapo
n'kanthu komwe kuti athe kulimanga. 11 Choncho wansembe Uriya
anamanga guwa lansembe molingana ndi chitsanzo chimene anamutu-
mizira Mfumu Ahazi kuchokera ku Damasiko ndipo anatsiriza kumanga
guwalo Ahazi asabwere kuchokera ku Damasiko kuja. 12 Mfumu itabwera
kuchokera ku Damasiko kuja ndi kuona guwalo, inasendera pafupi ndi
kupereka nsembe paguwapo. 13 Mfumu inapereka nsembe yopsereza ndi
nsembe ya chakudya. Inapereka nsembe yachakumwa ndi kuwaza magazi
a nsembe yake yachiyanjano paguwapo. 14 Guwa lamkuwa limene linali

pamaso pa Yehova analichotsa kutsogolo kwa nyumbayo, kulichotsa pakati
pa guwa latsopano ndi Nyumba ya Yehova ndi kukaliyika cha kumpoto
kwa guwa latsopanolo.
15 Pamenepo Mfumu Ahazi inalamula wansembe Uriya kuti, "Pa guwa
lalikulu latsopano uziperekapo nsembe yopsereza ya mmawa ndi nsembe
ya chakudya ya madzulo, nsembe yopsereza ya mfumu ndi nsembe yake
ya chakudya ndiponso nsembe za anthu onse a m'dziko, za chakudya
ndi chakumwa. Pa guwali uziwazapo magazi a nsembe zonse zopsereza
ndi nsembe zina zonse. Koma ine ndizigwiritsa ntchito guwa lansembe
lamkuwa pofuna kufunsira nzeru." 16 Ndipo wansembe Uriya anachita
monga analamulira Mfumu Ahazi.
17 Mfumu Ahazi anachotsa maferemu a maphaka nachotsapo mabeseni.
Iye anatsitsa mbiya yayikulu imene inali pamwamba pa ng'ombe
zamkuwa ndipo anayika pansi pa chiwundo cha miyala. 18 Iye anachotsa
kadenga ka pa Sabata kamene kanamangidwa m'kati mwa Nyumba ya
Yehova ndiponso anatseka chipata cholowera mfumu cha kunja kwa
nyumba ya Yehova pofuna kukondweretsa mfumu ya ku Asiriya.
19 Ntchito zina za Ahazi ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalembedwe
m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 20 Ahazi anamwalira ndipo
anayikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake mu Mzinda wa Davide.
Ndipo Hezekiya mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

# 17

### *Hoseya Mfumu Yotsiriza ya Israeli*

1 M'chaka cha 12 cha Ahazi mfumu ya Yuda, Hoseya mwana wa Ela
anakhala mfumu ya Israeli mu Samariya ndipo analamulira zaka zisanu
ndi zinayi. 2 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova, koma osafanana ndi
mafumu a Israeli amene ankalamulira iye asanalowe ufumuwo.
3 Salimenezeri mfumu ya ku Asiriya anabwera kudzathira nkhondo
Hoseya amene anali pansi pa ulamuliro wake ndipo ankapereka msonkho
kwa iyeyo. 4 Koma mfumu ya ku Asiriya inazindikira kuti Hoseya
akuwukira, pakuti Hoseyayo anali atatumiza nthumwi kwa So mfumu ya
Igupto ndiponso analeka kukhoma msonkho kwa mfumu ya ku Asiriya,
monga ankachitira chaka ndi chaka. Choncho Salimenezeri anagwira
Hoseya ndi kumuyika m'ndende. 5 Mfumu ya ku Asiriya inapita kukathira
nkhondo dziko lonse la Israeli ndipo inapita mpaka ku Samariya ndipo
inazinga mzindawo kwa zaka zitatu. 6 M'chaka chachisanu ndi chinayi cha
Hoseya, mfumu ya ku Asiriya inalanda Samariya ndipo inatenga Aisraeli
ndi kupita nawo ku Asiriya. Anakawakhazika ku Hala ndi Habori m'mbali
mwa mtsinje wa Gozani ndi m'mizinda ya Amedi.

### *Israeli Apita ku Ukapolo chifukwa cha Tchimo*

7 Zonsezi zinachitika chifukwa Aisraeli anachimwira Yehova Mulungu
wawo, amene anawatulutsa m'dziko la Igupto pansi pa ulamuliro wa
Farao mfumu ya Igupto. Iwo ankapembedza milungu ina, 8 ndiponso
ankatsatira miyambo ya anthu a mitundu imene Yehova anayichotsa
pamene iwo ankafika m'dzikomo pamodzinso ndi miyambo yonse imene
mafumu a Israeli anayambitsa. 9 Ndipo Aisraeli ankachita zoyipa
mwamseri kutsutsana ndi Yehova Mulungu wawo. Kuchokera ku nsanja
ya alonda mpaka ku mzinda wotetezedwa, m'mizinda yawo yonse
anamangamo malo opembedzeramo mafano. 10 Anayimika miyala ya

chipembedzo ndi mitengo ya mafano a Asera pa phiri lililonse lalitali
ndi pansi pa mtengo uliwonse wa masamba ambiri. 11 Pa malo ali-
wonse opembedzera mafano, anthuwa ankafukiza lubani monga momwe
ankachitira anthu a mitundu imene Yehova anayichotsa pamene iwo
ankafika. Iwo anachita zinthu zoyipa zomwe zinaputa mkwiyo wa Yehova.
12 Ndipo iwowo ankapembedza mafano ngakhale Yehova ananena kuti,
"Musadzachite zimenezi." 13 Yehova anachenjeza Israeli ndi Yuda kudzera
mwa aneneri ake onse ndi alosi kuti, "Lekani mchitidwe wanu woyipawo.
Mverani malamulo anga ndi malangizo anga potsatira zonse zolembedwa
m'malamulo a Mose, zimene ndinalamulira makolo anu kuti azimvere,
kudzera mwa aneneri, atumiki anga."

14 Koma anthuwa sanamvere ndipo anawumitsa khosi ngati momwe
analili makolo awo, amene sanadalire Yehova Mulungu wawo. 15 Anakana
malangizo ake ndi pangano anachita ndi makolo awo ndipo ananyoza
zochenjeza za Yehova. Iwo anatsatira mafano achabechabe nasanduka
achabechabe. Anthuwa anatsanzira mitundu ya anthu owazungulira
ngakhale kuti Yehova anawalamula kuti, "Musamachite zomwe iwo
amachita," koma iwo anachita zomwe Yehova anawaletsa.

16 Iwowo anasiya malamulo onse a Yehova Mulungu wawo, nadzi-
pangira mafano awiri osungunula a ana ang'ombe ndiponso fano la
Asera, napembedza zonse zamlengalenga ndi kutumikira Baala. 17 Ndipo
anadutsitsa m'moto ana awo aamuna ndi aakazi. Iwo ankawombeza
mawula, namachitanso zanyanga ndipo anadzipereka kuchita zoyipa
pamaso pa Yehova namukwiyitsa.

18 Choncho Yehova anakwiya nawo kwambiri Aisraeli ndipo anawa-
chotsa pamaso pake. Palibe amene anatsala kupatula fuko la Yuda lokha.
19 Yuda nayenso sanasunge malamulo a Yehova Mulungu wawo. Iwo
ankatsatira machitidwe amene Israeli anayambitsa. 20 Motero Yehova
anakana Aisraeli onse. Iye anawazunza nawapereka m'manja mwa anthu
ofunkha mpaka Iye atawachotseratu pamaso pake.

21 Yehova atang'amba Israeli kumuchotsa ku nyumba ya Davide,
Aisraeliwo anasankha Yeroboamu mwana wa Nebati kukhala mfumu
yawo. Yeroboamu ananyengerera Aisraeli kuti asatsatire Yehova ndipo
anawachimwitsa tchimo lalikulu. 22 Aisraeli anakakamira machimo onse
amene Yeroboamu anachita ndipo sanawasiye 23 mpaka pamene Yehova
anawachotsa pamaso pake monga anawachenjezera kudzera mwa atumiki
ake onse, aneneri. Choncho Aisraeli anachotsedwa m'dziko lawo kupita
ku ukapolo ku Asiriya ndipo ali komweko mpaka lero lino.

### *Anthu Achilendo Akhala mu Samariya*

24 Mfumu ya ku Asiriya inabweretsa anthu a ku Babuloni, Kuta, Awa,
Hamati ndi a ku Sefaravaimu kudzawakhazika m'mizinda ya Samariya
kulowa m'malo mwa Aisraeli. Iwo anatenga Samariya ndi kukhala
m'mizinda yake. 25 Iwo atayamba kukhala kumeneko, sanapembedze
Yehova choncho Yehova anatumiza mikango pakati pawo ndipo inapha
ena mwa iwo. 26 Tsono mfumu ya ku Asiriya inawuzidwa za nkhaniyi
kuti, "Anthu amene munawatumiza ndi kuwakhazika m'mizinda ya
Samariya sakudziwa chimene Mulungu wa dzikolo amafuna. Choncho
Iye watumiza mikango pakati pawo imene ikuwapha chifukwa anthuwo
sadziwa chimene Mulungu wa dzikolo amafuna."

27 Tsono mfumu ya ku Asiriya inalamula kuti, "Tengani wansembe
mmodzi mwa amene munawagwira ukapolo, mupite naye kumeneko

ndipo akakhale komweko nakaphunzitse anthu zimene Mulungu wa
dzikolo amafuna.” 28 Choncho mmodzi mwa ansembe amene anawatenga
ku Samariya anabwera kudzakhala ku Beteli ndipo ankaphunzitsa an-
thuwo kupembedza Yehova.

29 Koma mtundu uliwonse wa anthu unkapangabe mafano a milungu
yawoyawo m’mizinda yambiri imene anthuwo ankakhala, ndipo anayika
milunguyo m’nyumba za milungu zimene anthu a ku Samariya anamanga
ku malo opembedzera mafano. 30 Anthu a ku Babuloni anapanga Sukoti-
Benoti, anthu a ku Kuti anapanga Nerigali, ndipo anthu a ku Hamati
anapanga Asima; 31 Aava anapanga Nibihazi ndi Taritaki, ndipo Asefar-
avaimu ankawotcha ana awo pa moto ngati nsembe kwa Adirameleki
ndi Anameleki, milungu ya Asefaravaimu. 32 Iwo ankapembedza Yehova,
koma ankadzisankhira okha pakati pawo anthu wamba kuti akhale
ansembe awo ku nyumba za milungu za ku malo opembedzera mafano.
33 Iwowo ankapembedza Yehova, komanso ankatumikira milungu yawo
molingana ndi miyambo ya mitundu ya kumene ankachokera.

34 Mpaka lero lino iwo akupitirizabe kuchita zimene ankachita poyamba.
Sapembedza Yehova kapenanso kutsata malangizo ake ndi malamulo ake,
chiphunzitso chake monga mwa malamulo amene Yehova anawapereka
kwa zidzukulu za Yakobo, amene anamutcha Israeli. 35 Pamene Yehova
anachita pangano ndi Aisraeli, Iye anawalamula kuti, “Musapembedze
milungu ina kapena kuyigwadira iyo, kuyitumikira kapena kupereka
nsembe kwa iyoyo. 36 Koma Yehova amene anakutulutsani m’dziko
la Igupto ndi dzanja lake lamphamvu ndiye amene muyenera kumu-
pembedza. 37 Muyenera kusamalitsa nthawi zonse kusunga malangizo
anga ndi malemba anga, chiphunzitso ndi malamulo amene anakulem-
berani. Musapembedze milungu ina. 38 Musayiwale pangano limene
ndinapangana nanu ndipo musamapembedze milungu ina. 39 M’malo
mwake muzipembedza Yehova Mulungu wanu pakuti ndiye amene
adzakulanditsani m’dzanja la adani anu onse.”

40 Komabe iwo sanamvere ndipo anapitiriza kuchita zomwe ankachita
kale. 41 Ngakhale anthuwo ankapembedza Yehova, ankatumikiranso
mafano awo. Mpaka lero lino ana awo ndi zidzukulu zawo zikupitiriza
kuchita zomwe ankachita makolo awo.

# 18

*Hezekiya Mfumu ya Yuda*

1 M’chaka chachitatu cha Hoseya mwana wa Ela mfumu ya Israeli,
Hezekiya mwana wa Ahazi mfumu ya Yuda analowa ufumu. 2 Anakhala
mfumu ali ndi zaka 25 ndipo analamulira mu Yerusalemu zaka 29.
Amayi ake anali Abi, mwana wa Zekariya. 3 Iye anachita zolungama
pamaso pa Yehova monga anachitira Davide kholo lake. 4 Anachotsa malo
opembedzerako mafano, anaphwanya miyala yachipembedzo ndiponso
anadula mafano a Asera. Iye anaphwanya njoka yamkuwa imene Mose
anapanga, pakuti mpaka kufikira nthawi imeneyi Aisraeli amafukiza
lubani kwa njoka imeneyi. (Imatchedwa Nehusitani).

5 Hezekiya anadalira Yehova Mulungu wa Israeli. Kotero panalibe wina
wofanana naye pakati pa mafumu onse a Yuda, asanakhale mfumu kapena
atakhala kale mfumu. 6 Iye anakangamira Yehova ndipo sanamusiye koma
anasunga malamulo amene Yehova anapatsa Mose. 7 Ndipo Yehova anali

naye ndipo kulikonse kumene anapita zinthu zinkamuyendera bwino.
Iye anagalukira mfumu ya ku Asiriya ndipo sanayitumikirenso. 8 Iye
anakantha Afilisti kuyambira ku nsanja ya alonda mpaka ku mzinda
wotetezedwa. Anakafika mpaka ku Gaza ndi ku malire ake.
9 M'chaka chachinayi cha Mfumu Hezekiya, chimene chinali chaka
chachisanu ndi chiwiri cha Hoseya mwana wa Ela mfumu ya Israeli,
Salimenezeri, mfumu ya ku Asiriya anabwera kudzathira nkhondo mzinda
wa Samariya ndi kuwuzinga 10 Asiriya analanda mzindawu patatha zaka
zitatu. Choncho mzinda wa Samariya unalandidwa chaka chachisanu ndi
chimodzi cha Hezekiya, chimene chinali chaka chachisanu ndi chinayi
cha Hoseya mfumu ya Israeli. 11 Mfumu ya ku Asiriya inatenga Aisraeli
kupita nawo ku ukapolo ku Asiriya ndipo anakawakhazika ku Hala, ku
Habori pafupi ndi mtsinje wa Gozani ndi m'mizinda ya Amedi. 12 Izi
zinachitika chifukwa sanamvere zonena za Yehova Mulungu wawo, koma
anaphwanya pangano lake ndi zonse zimene Mose mtumiki wa Yehova
anawalamula. Iwo sanamvere malamulowo kapena kuwagwiritsa ntchito.
13 M'chaka chakhumi ndi chinayi cha ulamuliro wa Mfumu Hezekiya,
Senakeribu mfumu ya ku Asiriya anathira nkhondo mizinda yonse
yotetezedwa ya Yuda, nayilanda. 14 Choncho Hezekiya mfumu ya
Yuda anatumiza uthenga kwa mfumu ya ku Asiriya ku Lakisi wonena
kuti, "Ine ndalakwa. Chokani kuno ndipo ndidzakupatsani chilichonse
chimene munene." Mfumu ya ku Asiriya inalamula mfumu Hezekiya,
mfumu ya Yuda, kuti azipereka makilogalamu a siliva okwana 3,000 ndi
makilogalamu a golide 1,000. 15 Mfumu Hezekiya inapereka siliva yense
amene anapezeka m'Nyumba ya Yehova ndi m'nyumba zosungiramo
chuma cha mfumu.
16 Nthawi imeneyi Hezekiya mfumu ya Yuda anakanganula golide
amene anakuta zitseko ndi mphuthu za chipata cha Nyumba ya Yehova
namupereka kwa mfumu ya ku Asiriya.

### *Senakeribu Aopseza Yerusalemu*

17 Mfumu ya ku Asiriya inatuma Taritani, Rabusarisi ndi Rabusake
pamodzi ndi gulu lalikulu la ankhondo, kwa Mfumu Hezekiya ku
Yerusalemu kuchokera ku Lakisi. Iwo anafika ku Yerusalemu nakayima
pafupi ndi ngalande ya madzi yochokera ku Dziwe Lakumtunda, pa
msewu waukulu wopita ku malo a Munda wa Mmisiri Wochapa. 18 Iwo
anayitana mfumu, ndipo Eliyakimu mwana wa Hilikiya woyang'anira
nyumba ya mfumu, Sebina mlembi wa bwalo ndi Yowa mwana wa Asafu
mlembi wa zochitika anapita kwa anthuwo.
19 Ndipo Rabusake anawawuza kuti, "Kamuwuzeni Hezekiya kuti,
" 'Mfumu yayikulu, mfumu ya ku Asiriya ikunena kuti, 'Kodi
chikukulimbitsa mtima ndi chiyani?' 20 Iwe ukuti uli ndi luso ndiponso
mphamvu pa nkhondo, komatu ukuyankhula mawu opanda pake. Kodi
tsono iwe ukudalira yani kuti undiwukire ine? 21 Taona tsono, iwe
ukudalira Igupto, bango lothyokalo, limene limalasa m'manja mwa
munthu ngati waliyesa ndodo yoyendera! Umo ndi mmene Farao
mfumu ya ku Igupto imachitira aliyense amene akuyidalira.' " 22 Ndipo
ngati ukunena kwa ine kuti, "Ife tikudalira Yehova Mulungu wathu."
Kodi si Mulungu yemweyo amene nyumba zake ndi maguwa ake
Hezekiya anachotsa, nawuza anthu a ku Yuda ndi a ku Yerusalemu kuti,
"Muzipembedza pa guwa lansembe ili mu Yerusalemu?"

[23] " 'Ndipo tsopano bwera udzakambirane ndi mbuye wanga, mfumu
ya ku Asiriya: ine ndidzakupatsa akavalo 2,000 ngati ungathe kupeza
okwerapo! [24] Ungathe bwanji kugonjetsa ngakhale mmodzi mwa
akazembe ang'onoang'ono a mbuye wanga, pamene ukudalira Igupto
kuti akupatse magaleta ndi anthu okwera pa akavalo? [25] Kuwonjezera
pamenepa, kodi ine ndabwera kudzathira nkhondo ndi kuwononga
malo ano popanda chilolezo cha Yehova? Yehova mwini ndiye
anandiwuza kuti ndidzathire nkhondo ndi kuwononga dziko lino.' "

[26] Pamenepo Eliyakimu mwana wa Hilikiya, Sebina ndi Yowa anawuza
Rabusakeyo kuti, "Chonde yankhulani kwa atumiki anufe m'Chiaramu,
popeza timachimva. Musayankhule nafe mu Chihebri kuopa kuti anthu
onse amene ali pa khomapa angamve."

[27] Koma Rabusake anayankha kuti, "Kodi mbuye wanga wandituma
kuti ndidzanene zinthu izi kwa mbuye wanu yekha ndi inu nokha basi?
Ayi, komanso kwa anthu amene akhala pa khomawa. Iwowa adzadya
chimbudzi chawo chomwe ndi kumwa mkodzo wawo womwe monga
momwe mudzachitire inuyonso."

[28] Tsono Rabusake anayimirira nafuwula mu Chihebri kuti, "Imvani
mawu a mfumu yayikulu, mfumu ya ku Asiriya! [29] Zimene mfumu
ikunena ndi izi: 'Musalole kuti Hezekiya akunamizeni. Iye sangakupulu-
mutseni m'dzanja langa. [30] Hezekiya asakukakamizeni kudalira Yehova
ndi mawu akuti, 'Ndithu, Yehova adzatipulumutsa; ndipo sadzapereka
mzindawu m'dzanja la mfumu ya ku Asiriya.'

[31] "Musamumvere Hezekiya. Zimene mfumu ya ku Asiriya ikunena ndi
izi: Pangani mtendere ndi ine ndipo mutuluke mu mzinda. Mukatero
aliyense wa inu adzadya mphesa ndi nkhuyu za m'munda mwake
ndiponso adzamwa madzi a m'chitsime chake, [32] mpaka nditabwera
kudzakutengani kupita ku dziko lofanana ndi lanuli, dziko la tirigu ndi
vinyo watsopano, dziko la chakudya ndi minda ya mipesa, dziko la
mitengo ya olivi ndi uchi. Sankhani moyo osati imfa!

"Musamvere zonena Hezekiya, pakuti iye akukusocheretsani ponena
kuti, 'Yehova adzatipulumutsa.' [33] Kodi mulungu wa anthu a mtundu wina
uliwonse wapulumutsapo dziko lake m'dzanja la mfumu ya ku Asiriya?
[34] Kodi ili kuti milungu ya Hamati ndi Aripadi? Ili kuti milungu ya
Sefaravaimu, Hena ndi Ivani? Kodi inapulumutsa Samariya m'dzanja
langa? [35] Kodi ndi milungu iti mwa milungu yonse ya mayiko awa
amene anapulumutsa dziko lake m'dzanja langa? Nanga tsono Yehova
adzapulumutsa Yerusalemu m'dzanja langa motani?"

[36] Koma anthu anakhala chete ndipo sanayankhepo kanthu, chifukwa
mfumu inawalamula kuti, "Musayankhe."

[37] Pamenepo anthu atatu aja Eliyakimu, mwana wa Hilikiya amene
ankayang'anira nyumba ya mfumu, Sebina mlembi wa bwalo ndi Yowa
mwana wa Asafu, mlembi wa zochitika anapita kwa Hezekiya atang'amba
zovala zawo ndipo anamuwuza Hezekiya zonse zimene anayankhula
Rabusake uja.

# 19

*Kupulumutsidwa kwa Yerusalemu*

[1] Mfumu Hezekiya atamva zimenezi, anang'amba zovala zake navala
chiguduli ndipo analowa m'Nyumba ya Yehova. [2] Iye anatuma Eliyakimu,

woyang'anira nyumba ya mfumu, Sebina mlembi wa bwalo ndi ansembe
akuluakulu, onse atavala ziguduli, kwa mneneri Yesaya mwana wa Amozi.
3 Iwo anamuwuza kuti, "Hezekiya akunena kuti, 'Lero ndi tsiku lamavuto,
lachilango ndi lamanyazi. Ife lero tili ngati mayi woyembekezera amene
pofika nthawi yoti achire akupezeka kuti alibe mphamvu zoberekera.
4 Mwina Yehova Mulungu wanu adzamva mawu onse a Rabusake amene
mbuye wake, mfumu ya ku Asiriya anamutuma kudzanyoza Mulungu
wamoyo, ndipo Mulunguyo adzamulanga chifukwa cha mawu amene
Yehova Mulungu wanu wamva. Choncho pemphererani anthu otsala
amene akanali ndi moyo.' "

5 Akuluakulu a Mfumu Hezekiya atafika kwa Yesaya, 6 Yesaya
anawawuza kuti, "Kawuzeni mbuye wanu kuti, 'Yehova akunena kuti:
Usachite mantha ndi zimene wamva, mawu amene nthumwi za mfumu
ya ku Asiriya zandinyoza nawo Ine. 7 Tamverani! Ine ndidzayika mwa
mfumuyo mzimu wina kotero kuti akadzamva mphekesera ya nkhondo,
adzabwerera ku dziko lake ndipo Ine ndidzachititsa kuti aphedwe ndi
lupanga kwawo komweko.' "

8 Rabusake atamva kuti mfumu ya ku Asiriya yachoka ku Lakisi, iye
anabwerera m'mbuyo ndipo anakapeza mfumu ikuchita nkhondo ndi
mzinda wa Libina.

9 Nthawi imeneyi Senakeribu analandira uthenga wakuti Tirihaka,
mfumu ya ku Kusi, akubwera kudzachita naye nkhondo. Choncho iye
anatumanso amithenga kwa Hezekiya ndi mawu awa: 10 "Kawuzeni
Hezekiya mfumu ya Yuda kuti: Usalole kuti Mulungu amene ukumudalira
akupusitse ponena kuti, 'Yerusalemu sadzaperekedwa m'manja mwa
mfumu ya ku Asiriya.' 11 Ndithu iwe unamva chimene mafumu a Asiriya
anachita ku mayiko ena onse, kuti anawawononga kotheratu. Ndipo kodi
iwe n'kupulumuka? 12 Kodi milungu ya mitundu imene makolo anga
anayigonjetsa, milungu ya anthu a ku Gozani, Harani, Rezefi ndi Aedeni
amene anali ku Teli Asara, inawapulumutsa? 13 Kodi mafumu a Hamati,
Aripadi ndi mafumu a mizinda ya Sefaravaimu, Hena ndi Iva, ali kuti?"

### *Pemphero la Hezekiya*

14 Hezekiya analandira kalata kwa amithenga aja nayiwerenga.
Pomwepo anapita ku Nyumba ya Yehova nayika kalatayo pamaso pa
Yehova. 15 Ndipo Hezekiya anapemphera kwa Yehova nati, "Inu Yehova
Mulungu wa Israeli, Inu amene mumakhala pa Akerubi, Inu nokha ndinu
Mulungu wolamulira maufumu onse a dziko lapansi. Inu munalenga
kumwamba ndi dziko lapansi. 16 Inu Yehova, tcherani khutu lanu ndipo
mumve Yehova tsekulani maso anu ndipo muone, imvani mawu onse
amene Senakeribu watumiza kunyoza Inu Mulungu wamoyo.

17 "Inu Yehova, n'zoonadi kuti mafumu a Asiriya anawononga mitundu
iyi ndi mayiko awo. 18 Iwo anaponya milungu yawo pa moto ndi
kuyiwononga pakuti sinali milungu koma mitengo ndi miyala chabe,
yopangidwa ndi anthu. 19 Ndipo tsopano Inu Yehova Mulungu wathu,
tipulumutseni ndithu m'dzanja lake, kuti maufumu onse a dziko lapansi
adziwe kuti Inu nokha, Inu Yehova, ndinu Mulungu."

### *Yankho la Mulungu Kudzera mwa Yesaya*

20 Ndipo Yesaya mwana wa Amozi anatumiza uthenga kwa Hezekiya
wakuti, "Yehova Mulungu wa Israeli akuti, 'Ndamva pemphero lako

lonena za Senakeribu mfumu ya ku Asiriya.' " 21 Mawu amene Yehova
wayankhula wotsutsana naye ndi awa:
"Namwali wa Ziyoni
akukunyoza ndi kukuseka iwe.
Mwana wamkazi wa Yerusalemu
akupukusa mutu wake kumbuyo kwako.
22 Kodi iweyo wanyoza ndi kuchitira chipongwe yani?
Kodi ndani amene wamufuwulira mawu ako
ndi kumuyang'ana monyada?
Wachitiratu izi Woyera wa Israeli!
23 Kudzera mwa amithenga ako
wonyoza Ambuye.
Ndipo wanena kuti,
'Ndi magaleta ochuluka
ndinakwera mapiri ataliatali,
pa msonga za mapiri a Lebanoni.
Ndigwetsa mitengo yake ya mkungudza yayitali kwambiri,
mitengo yake ya payini yabwino kwambiri.
Ndalowanso m'kati mwake mwenimweni,
mwa nkhalango yake yowirira kwambiri.
24 Ndakumba zitsime ku mayiko achilendo
ndipo ndinamwa madzi a kumeneko.
Ndi mapazi anga
ndawumitsa mitsinje yonse ya ku Igupto.' "

25 " 'Kodi sunamvepo?
Zimenezi ndinazikhazikitsa kalekale.
Ndinazikonzeratu masiku amakedzana;
tsopano ndachita kuti zichitikedi,
iwe kwako kunali kungosandutsa mizinda yotetezedwa
kukhala milu ya miyala.
26 Anthu a kumeneko ndi opanda mphamvu,
athedwa nzeru ndipo ali ndi manyazi.
Ali ngati mbewu za m'munda,
ngati udzu wanthete,
ali ngati udzu womera pa denga,
umene umawuma usanakule n'komwe.' "

27 " 'Koma Ine ndimadziwa kukhala kwako,
kutuluka kwako ndi kulowa kwako,
ndi mkwiyo wako pa Ine.
28 Chifukwa chakuti wandikwiyira
ndipo ndamva za mwano wako,
ndidzakola mphuno yako ndi mbedza
ndi kuyika chitsulo changa m'kamwa mwako,
ndipo ndidzakubweza pokudzeretsa
njira yomwe unadzera pobwera.'
29 "Koma iwe Hezekiya, chizindikiro chako chidzakhala ichi:
"Chaka chino mudzadya tirigu wamphulumukwa,
ndipo chaka chamawa mudzadya tirigu wongodzimerera.
Koma chaka chachitatu mudzadzala ndi kukolola,
mudzawoka mphesa ndipo mudzadya zipatso zake.
30 Anthu a nyumba ya Yuda amene adzatsale

adzazika mizu ndi kubereka zipatso.
31 Pakuti ku Yerusalemu kudzachokera anthu otsala,
ndi ku phiri la Ziyoni kudzachokera gulu la anthu opulumuka."
"Changu cha Yehova Wamphamvuzonse chidzachita zimenezi.

32 "Choncho chimene Yehova akunena za mfumu ya ku Asiriya ndi ichi:
" 'Iye sadzalowa mu mzinda umenewu
kapena kuponyamo muvi.
Sadzayandikira mzindawu ndi zishango zake
kapena kumanga nthumbira ya nkhondo.
33 Adzabwerera potsata njira imene anadzera pobwera;
sadzalowa mu mzinda umenewu,
akutero Yehova.
34 Ndidzateteza mzinda umenewu kuwupulumutsa,
chifukwa cha Ine mwini ndiponso chifukwa cha Davide mtumiki wanga.' "

35 Usiku umenewo mngelo wa Yehova anapita ku misasa ya ku Asiriya
ndi kupha ankhondo 185,000. Ndipo pamene anthu anadzuka mmawa,
taonani, mitembo inali ngundangunda! 36 Choncho Senakeribu mfumu
ya ku Asiriya anapasula misasa ndi kuchoka. Anabwerera ku Ninive
nakakhala kumeneko.
37 Tsiku lina, pamene Senakeribu ankapembedza m'nyumba ya Nisiroki
mulungu wake, ana ake Adirameleki ndi Sarezeri anamupha ndi lupanga
ndipo anathawira ku dziko la Ararati. Tsono Esrahadoni, mwana wake,
analowa ufumu m'malo mwake.

# 20

### *Kudwala kwa Hezekiya*

1 Masiku amenewo Hezekiya anadwala ndipo anali pafupi kufa.
Mneneri Yesaya, mwana wa Amozi anapita kukamuona ndipo anamuwuza
kuti, "Yehova akuti: Konza nyumba yako chifukwa umwalira ndipo
suchira."
2 Hezekiya anatembenuka nayang'ana ku khoma ndipo anapemphera
kwa Yehova kuti, 3 "Inu Yehova, kumbukirani ndithu mmene ndayendera
mokhulupirika ndi mtima wonse ndipo ndachita zolungama pamaso
panu." Hezekiya analira kwambiri.
4 Yesaya asanatuluke m'bwalo lapakati, Yehova anayankhula kuti,
5 "Bwerera, kamuwuze Hezekiya mtsogoleri wa anthu anga kuti, 'Yehova
Mulungu wa Davide kholo lako akuti: Ndamva pemphero lako ndipo
misozi yako ndayiona ndipo ndidzakuchiritsa. Tsiku lachitatu kuchokera
lero udzapita ku Nyumba ya Yehova. 6 Ndidzawonjezera zaka khumi ndi
zisanu pa moyo wako. Ndidzakupulumutsa iwe pamodzi ndi mzinda ume-
newu m'dzanja la mfumu ya ku Asiriya. Ndidzateteza mzinda umenewu
chifukwa cha Ine mwini ndiponso chifukwa cha Davide mtumiki wanga.' "
7 Pamenepo Yesaya anati, "Konzani phala lankhuyu." Iwo anakonza
phalalo nalipaka pa chithupsacho ndipo Hezekiya anachira.
8 Tsono Hezekiya anafunsa Yesaya kuti, "Kodi padzakhala chizindikiro
chanji choonetsa kuti Yehova adzandichiritsa ndi kuti ndidzapita ku
Nyumba ya Yehova pa tsiku lachitatu kuchokera lero lino?"
9 Yesaya anayankha kuti, "Chizindikiro cha Yehova chosonyeza kuti
Iye adzachita chimene walonjeza ndi ichi: Kodi chithunzithunzi chipite
patsogolo kapena chibwerere pambuyo makwerero khumi?"

10 Hezekiya anati, “N’chapafupi kuti chithunzithunzi chipite patso-
golo makwerero khumi, kulekana n’kuti chithunzithunzicho chibwerere
m’mbuyo makwerero khumi.”
11 Pamenepo mneneri Yesaya anapemphera kwa Yehova ndipo Yehova
anachititsa kuti chithunzithunzi chibwerere m’mbuyo makwerero khumi
pa makwerero amene mfumu Ahazi anamanga.

### *Akazembe Ochokera ku Babuloni*

12 Pa nthawi imeneyo Merodaki-Baladani mwana wa Baladani mfumu
ya Babuloni anatumiza amithenga kwa Hezekiya kukapereka makalata
ndi mphatso, chifukwa n’kuti atamva za kudwala kwa Hezekiyayo.
13 Hezekiya analandira amithengawo ndipo anawaonetsa zonse zimene zi-
nali m’nyumba zake zosungiramo chuma. Anawaonetsa siliva, golide, zo-
nunkhiritsa zakudya ndi mafuta abwino kwambiri, zida zake zankhondo
ndiponso china chilichonse chimene chinali mosungiramo zinthu zake.
Panalibe chinthu m’nyumba yake yaufumu kapena mu ufumu wake
wonse chimene Hezekiya sanawaonetse.
14 Tsono mneneri Yesaya anapita kwa Mfumu Hezekiya namufunsa kuti,
“Kodi anthu aja anakuwuzani zotani ndipo anachokera kuti?”
Hezekiya anayankha kuti, “Anachokera ku dziko lakutali, ku Babuloni.”
15 Mneneriyo anafunsa kuti, “Kodi anaona chiyani m’nyumba yanu
yaufumu?”
Hezekiya anayankha kuti, “Anaona china chilichonse m’nyumba yanga
yaufumu ndipo palibe ndi chinthu chimodzi chomwe chimene sindi-
nawaonetse m’nyumba zanga zosungiramo chuma.”
16 Pamenepo Yesaya anawuza Hezekiya kuti, “Imvani zimene Yehova
akunena: 17 Taonani, masiku akubwera ndithu pamene zonse za
m’nyumba yanu yaufumu, zonse zimene makolo anu anazisunga mpaka
lero, zidzatengedwa kupita ku Babuloni. Palibe chimene chidzatsale,
akutero Yehova. 18 Ndipo ena mwa ana anu omwe, amene mudzabereke
adzatengedwa ndipo adzawasandutsa anthu ofulidwa m’nyumba yau-
fumu ya mfumu ya Babuloni.”
19 Hezekiya anayankha kuti, “Mawu a Yehova amene mwayankhulawa
ndi abwino. Pakuti iye ankaganiza kuti, ‘Kodi pa nthawi yanga sipadza-
khala mtendere ndi bata?’ ”
20 Ntchito zina za Hezekiya ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m’buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 21 Hezekiya anamwalira
nagona pamodzi ndi makolo ake. Ndipo Manase mwana wake analowa
ufumu m’malo mwake.

# 21

### *Manase Mfumu ya Yuda*

1 Manase anakhala mfumu ali ndi zaka khumi ndi ziwiri ndipo anala-
mulira mu Yerusalemu zaka 55. Amayi ake anali Hefiziba. 2 Iye anachita
zoyipa pamaso pa Yehova, potsatira mchitidwe wonyansa wa mitundu
imene Yehova anayipirikitsa pofika Aisraeli. 3 Iyetu anamanganso malo
opembedzera mafano amene Hezekiya abambo ake anawawononga.
Anamangira Baala maguwa a nsembe ndi mtengo wa fano la Asera monga
anachitira Ahabu mfumu ya Israeli ndipo ankapembedza zolengedwa
zonse zamlengalenga. 4 Anamanga maguwa ansembewa m’Nyumba ya
Yehova, m’mene Yehova ananena kuti, “Mu Yerusalemu ndidzayikamo

Dzina langa.” 5 M’mabwalo onse awiri a Nyumba ya Yehova, Manase
anamangamo maguwa opembedzerapo zinthu zamlengalenga. 6 Iye
anapsereza mwana wake pa moto ngati nsembe, ankachita za matsenga,
ankawombeza mawula, ankapita kwa woyankhula ndi mizimu ya anthu
akufa ndiponso ankapembedza mizimu. Iyeyo anachita zoyipa zambiri
pamaso pa Yehova ndipo anakwiyitsa Yehovayo.

7 Iye anatenga fano losema la Asera limene analipanga ndi kuliyika
m’Nyumba ya Yehova, Nyumba imene Yehova ananena kwa Davide ndi
mwana wake Solomoni kuti, “M’nyumba iyi ndi mu Yerusalemu ndiwo
malo amene ndasankha pakati pa mafuko onse a Aisraeli kuyikamo
Dzina langa kwamuyaya. 8 Sindidzalola kuti Aisraeli achotsedwe m’dziko
lawo limene ndinapatsa makolo awo ngati iwowo adzasamala kuchita
zinthu zonse zimene ndinawalamula ndi kusunga malamulo onse amene
mtumiki wanga Mose anawapatsa.” 9 Koma anthu sanamvere. Manase
anawasocheretsa, kotero kuti anachita zoyipa zambiri kupambana anthu
a mitundu ina amene Yehova anawawononga pamene Aisraeli ankafika.

10 Yehova anayankhula kudzera mwa atumiki ake, aneneri kuti,
11 “Manase mfumu ya Yuda wachita machimo onyansawa ndipo wachita
zoyipa kupambana Aamori amene analipo kale iye asanabadwe ndi
kuchimwitsa anthu a ku Yuda ndi mafano ake. 12 Choncho Yehova
Mulungu wa Israeli akuti, ‘Taonani, ndikubweretsa pa Yerusalemu ndi
Yuda mavuto akuti aliyense amene adzawamve adzathedwa nzeru.
13 Ndidzalanga Yerusalemu ndi Yuda pogwiritsa ntchito muyeso umene nd-
inalangira Samariya ndi Ahabu pamodzi ndi nyumba yake. Ndidzayeretsa
Yerusalemu monga mmene munthu amachitira popukuta mbale ndipo
atayipukuta amayivundikira pansi. 14 Ndidzawataya anthu otsala amene
ndi cholowa changa ndipo ndidzawapereka m’manja mwa adani awo.
Adzachotsedwa ndipo adaniwo adzawalanda zinthu zonse 15 chifukwa
anachita zoyipa pamaso panga ndipo akhala akundikwiyitsa kuchokera
tsiku limene makolo awo anatuluka mu Igupto mpaka lero lino.’ ”

16 Kuwonjezera apo, Manase anakhetsa kwambiri magazi a anthu
osalakwa mpaka magaziwo kuyenderera mu Yerusalemu kuyambira
mbali ina mpaka mbali ina, kuphatikiza pa kuchimwitsa Yuda, kotero kuti
anthu anachita zoyipa pamaso pa Yehova.

17 Ntchito zina za Manase ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m’buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 18 Manase anagona ndi
makolo ake ndipo anayikidwa m’manda m’munda wa Uza, ku nyumba
yaufumu. Ndipo Amoni mwana wake analowa ufumu m’malo mwake.

### *Amoni Mfumu ya Yuda*

19 Amoni anakhala mfumu ali ndi zaka 22 ndipo analamulira mu
Yerusalemu zaka ziwiri. Amayi ake anali Mesulemeti mwana wa Haruzi,
wochokera ku Yotiba. 20 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova monga
anachitira Manase abambo ake. 21 Anatsatira makhalidwe onse a abambo
ake. Ankapembedza mafano amene abambo akewo ankawapembedza
ndipo ankawagwadira. 22 Iyeyo anasiya Yehova Mulungu wa makolo ake
ndipo sanayende m’njira ya Yehova.

23 Nduna za Amoni zinamuchita chiwembu ndipo zinamupha m’nyumba
yake. 24 Koma anthu a m’dzikomo anapha onse amene anachitira
chiwembu Mfumu Amoni, nayika Yosiya mwana wake kukhala mfumu
m’malo mwake.

[25] Ntchito zina za Amoni ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? [26] Iye anayikidwa m'manda
ake m'munda wa Uza. Ndipo Yosiya mwana wake analowa ufumu m'malo
mwake.

# 22

*Buku la Malamulo Lipezeka*

[1] Yosiya anakhala mfumu ali ndi zaka zisanu ndi zitatu ndipo anala-
mulira mu Yerusalemu zaka 31. Amayi ake anali Yedida mwana wa Adaiya
wochokera ku Bozikati. [2] Iye anachita zolungama pamaso pa Yehova ndipo
anayenda m'njira zonse za Davide kholo lake, osatembenukira kumanja
kapena kumanzere.

[3] M'chaka cha 18 cha ufumu wake, Mfumu Yosiya anatuma mlembi wa
nyumba ya mfumu, Safani, mwana wa Azariya, mwana wa Mesulamu,
ku Nyumba ya Yehova. Iye anati, [4] "Pita kwa mkulu wa ansembe
Hilikiya ndipo ukamuwuze kuti awerenge ndalama zimene anthu abwera
nazo ku Nyumba ya Yehova, zimene alonda a pa khomo anasonkhanitsa
kwa anthu. [5] Ndalamazo azipereke kwa anthu amene asankhidwa kuti
ayang'anire ntchito ya Nyumba ya Yehova. Ndipo anthu amenewa
azilipira antchito amene akukonzanso Nyumba ya Yehova, [6] amisiri a
matabwa, amisiri omanga ndi amisiri a miyala. Iwo akagulenso matabwa
ndi miyala yosemedwa kuti akonzere Nyumba ya Yehova. [7] Koma
anthu amene apatsidwa ndalama zolipira antchito okonza Nyumbayo
asawafunse za kagwiritsidwe ntchito ka ndalamazo, popeza ndi anthu
wokhulupirika."

[8] Mkulu wa ansembe Hilikiya anawuza Safani, mlembiyo kuti, "Ndapeza
Buku la Malamulo m'Nyumba ya Yehova." Anapereka bukulo kwa Safani
amene analiwerenga. [9] Ndipo Safani mlembi uja, anapita nakafotokozera
mfumu kuti, "Atumiki anu apereka ndalama zija zinali m'Nyumba ya
Yehova kwa anthu amene akugwira ntchito ndi kuyang'anira ntchito
yokonza Nyumba ya Yehova." [10] Kenaka Safani mlembiyo, anafotokozera
mfumu kuti, "Wansembe Hilikiya wandipatsa buku." Ndipo Safani
analiwerenga pamaso pa mfumu.

[11] Mfumu itamva mawu a m'Buku la Malamulo, inang'amba zovala
zake. [12] Iyo inalamula wansembe Hilikiya, Ahikamu mwana wa Safani,
Akibo mwana wa Mikaya, Safani mlembi uja ndi Asaiya mtumiki wa
mfumu, kuti, [13] "Pitani mukafunse Yehova m'malo mwanga ndi m'malo
mwa anthu onse a m'dziko la Yuda, za zomwe zalembedwa m'buku
limene lapezekali. Mkwiyo wa Yehova ndi waukulu kwambiri pa ife
ndipo watiyakira chifukwa makolo athu sanamvere mawu a buku ili. Iwo
sanachite molingana ndi zonse zimene zalembedwa m'menemu zokhudza
ife."

[14] Choncho Hilikiya wansembe, Ahikamu, Akibo, Safani ndi Asaiya
anapita kukayankhula ndi Hulida, mneneri wamkazi, mkazi wa Salumu
mwana wa Tikiva, mwana wa Harihasi, wosunga zovala zaufumu.
Mneneri wamkaziyu ankakhala mu Yerusalemu, ku chigawo chachiwiri
cha mzindawo.

[15] Ndipo iye anawawuza kuti, "Yehova Mulungu wa Israeli akuti:
Kamuwuzeni munthu amene wakutumani kwa ine kuti, [16] 'Ichi ndi
chimene Yehova akunena: Taonani, ndidzabweretsa mavuto pa malo
ano ndi pa anthu ake, molingana ndi zonse zimene zalembedwa m'buku

limene mfumu ya Yuda yawerenga. 17 Chifukwa anthuwo andisiya Ine
ndi kumafukiza lubani kwa milungu ina nandikwiyitsa ndi mafano onse
amene manja awo anapanga, mkwiyo wanga udzayaka pa malo ano
ndipo sudzazimitsidwa.' 18 Koma mfumu ya Yuda imene inakutumani
kuti mudzafunse kwa Yehova kayiwuzeni kuti, 'Ichi ndi chimene Yehova
Mulungu wa Israeli akunena molingana ndi mawu amene unamva:
19 Chifukwa unasweka mtima ndi kudzichepetsa wekha pamaso pa
Yehova, pamene unamva zomwe zinayankhulidwa zotsutsana ndi malo
ano ndi anthu ake, kuti adzakhala otembereredwa nasanduka bwinja,
ndiponso chifukwa unang'amba zovala ndi kulira pamaso panga, ndamva
pemphero lako, akutero Yehova. 20 Choncho taona, Ine ndidzakutenga
kupita kwa makolo ako ndipo udzayikidwa m'manda mwako mwamtendere. Maso ako sadzaona mavuto onse amene ndidzabweretse pamalo
pano.' "

Ndipo anthu aja anabwerera nakafotokoza mawu amenewa kwa mfumu.

# 23

## *Yosiya Akonzanso Pangano*

1 Pamenepo mfumu inayitanitsa akuluakulu onse a ku Yuda ndi
Yerusalemu. 2 Mfumuyo inapita ku Nyumba ya Yehova pamodzi ndi
anthu onse a ku Yuda, ndi onse okhala mu Yerusalemu, ansembe ndi aneneri, ndiponso anthu ena onse kuyambira wamng'ono mpaka wamkulu. Mfumuyo inawerenga mawu onse a m'Buku la Chipangano
limene linapezeka m'Nyumba ya Yehova, anthu onse akumva. 3 Mfumu
inayimirira pambali pa chipilala ndi kuchita pangano pamaso pa Yehova kuti idzatsatira Yehova ndi kusunga malamulo, mawu ndi malangizo ake ndi mtima wonse ndi moyo wonse, kukwaniritsa mawu a m'panganoli, olembedwa m'bukuli. Pamenepo anthu onse anadzipereka kutsatira panganoli.

4 Mfumu inalamula wansembe wamkulu Hilikiya, ansembe othandizana naye ndi alonda a pa khomo kuti achotse m'Nyumba ya Yehova ziwiya zonse zopembedzera Baala ndi Asera ndiponso mafano a zinthu zamlengalenga. Yosiya anazitentha kunja kwa Yerusalemu, ku minda ya ku
Chigwa cha Kidroni ndipo phulusa lake anapita nalo ku Beteli. 5 Iye
anachotsa ansembe a mafano amene anayikidwa ndi mafumu a Yuda kuti azifukiza lubani ku malo opembedzera mafano a ku mizinda ya ku Yuda ndi kumalo ozungulira Yerusalemu, amene ankafukiza lubani kwa Baala,
dzuwa, mwezi, nyenyezi ndi zinthu zonse zamlengalenga. 6 Anachotsa
fano la Asera m'Nyumba ya Yehova napita nalo kunja kwa Yerusalemu, ku Chigwa cha Kidroni, nalitentha kumeneko. Anapera fanolo ndi kukataya
phulusa lake pa manda a anthu wamba. 7 Iye anagwetsanso tinyumba ta
ochita zachiwerewere, timene tinali m'Nyumba ya Yehova, kumene akazi ankalukirako mikanjo yovala popembedza Asera.

8 Yosiya anabweretsanso ansembe onse kuchokera m'mizinda ya Yuda, nawononga malo opembedzera mafano, kuyambira ku Geba mpaka ku Beeriseba, kumene ansembe ankafukizako lubani. Anagwetsa nyumba za milungu zimene zinali pa chipata cha Yoswa, bwanamkubwa wa
mzindawo, kumanzere kwa chipata cha mzinda. 9 Ngakhale kuti ansembe
a ku malo opembedzera mafanowo sanawalole kuti atumikire pa guwa

lansembe la Yehova mu Yerusalemu, koma ankadya buledi wopanda yisiti
pamodzi ndi ansembe anzawo.

10 Mfumu Yosiya anawononganso Tofeti, amene anali ku Chigwa cha
Hinomu, kuti wina aliyense asagwiritse ntchito malowo popereka mwana
wake wamwamuna kapena wamkazi pa moto kwa Moleki. 11 Anachotsa pa
chipata cholowera ku Nyumba ya Yehova akavalo amene mafumu a Yuda
anawapereka ngati nsembe kwa dzuwa. Akavalo anali pafupi ndi bwalo
la chipinda cha mkulu wina wotchedwa Natani-Meleki. Ndipo Yosiya
anatentha magaleta opembedzera dzuwa.

12 Anagwetsa maguwa amene mafumu a Yuda anawamanga pa denga
pafupi ndi chipinda chapamwamba cha Ahazi, ndiponso maguwa amene
Manase anamanga m'mabwalo awiri a Nyumba ya Yehova. Yosiya anawa-
chotsa kumeneko nawaphwanya ndi kutaya zidutswa zake m'Chigwa cha
Kidroni. 13 Mfumuyo inawononga malo opembedzera mafano amene ali
kummawa kwa Yerusalemu cha kumpoto kwa Phiri la Chiwonongeko.
Maguwawa Solomoni mfumu ya Israeli inamangira Asitoreti, fano lalikazi
lonyansa la Asidoni, Kemosi, fano lonyansa la Amowabu, ndi Moleki,
fano lonyansa la anthu a ku Amoni. 14 Yosiya anaphwanya miyala
ya chipembedzo ndiponso anadula mitengo ya fano la Asera ndipo
anakwirira malowo ndi mafupa a anthu.

15 Ngakhalenso guwa lansembe la ku Beteli, malo opembedzera mafano
amene anapanga Yeroboamu mwana wa Nebati, amene anachimwitsa
Israeli, Yosiya anawononga guwalo ndi malo opembedzera mafanowo.
Iye anatentha malo opembedzera mafanowo ndi kuwapera ndipo ana-
tenthanso fano la Asera. 16 Kenaka Yosiya anayang'anayang'ana ndipo
ataona manda amene anali pomwepo, m'mbali mwa phiri, analamula
kuti afukule mandawo ndi kutulutsa mafupa kuti awatenthe paguwapo
kuti alidetse, potsatira mawu a Yehova amene munthu wa Mulungu
analoseratu za zimenezi.
17 Mfumu inafunsa kuti, "Kodi chizindikiro cha manda chimene
ndikuwaonawo ndi chayani?"

Anthu a mu mzindamo anayankha kuti, "Ndi chizindikiro cha manda a
munthu wa Mulungu wochokera ku Yuda amene ananeneratu zimene inu
mwalichita guwa lansembe la Beteli."

18 Mfumuyo inati, "Alekeni manda amenewo, munthu asachotse mafupa
ake." Choncho anawasiya mafupa akewo pamodzi ndi mafupa a mneneri
wa ku Samariya uja.

19 Monga momwe Yosiya anachitira ku Beteli, anachotsa ndi kuwononga
nyumba za milungu zonse ndi malo opembedzera mafano amene mafumu
anamanga m'mizinda ya ku Samariya omwe anakwiyitsa Yehova. 20 Yosiya
anapha ansembe onse amene ankatumikira ku malo opembedzera
mafano, anawaphera pa maguwa awo ndi kutentha mafupa awo. Kenaka
iye anapita ku Yerusalemu.

21 Mfumu inalamula anthu onse kuti, "Chitani Chikondwerero cha
Paska kulemekeza Yehova Mulungu wanu, motsatira zomwe zalembedwa
m'Buku la Chipangano." 22 Paska yotere inali isanachitikepo kuyambira
nthawi ya oweruza amene anatsogolera Israeli, kapenanso nthawi yonse
ya mafumu a Yuda sipanachitikenso Paska ngati imeneyo. 23 Koma
m'chaka cha 18 cha Mfumu Yosiya, Paska imeneyi anachitira Yehova mu
Yerusalemu.

24 Kuwonjezera apa, Yosiya anachotsa anthu a mawula, woyankhula
ndi mizimu ya anthu akufa, milungu ya m'nyumba, mafano ndiponso
zinthu zonse zonyansa zopezeka mu Yuda ndi Yerusalemu. Iye
anachita izi pokwaniritsa lamulo lolembedwa m'buku limene Hilikiya
analipeza m'Nyumba ya Yehova. 25 Yosiyayo asanalowe ufumu, ngakhale
atamwalira, panalibenso mfumu ina yofanana naye imene inatembe-
nukira kwa Yehova monga anachitira, ndi mtima wake wonse, ndi moyo
wake wonse, ndi mphamvu zake zonse, motsatira Malamulo onse a Mose.

26 Komabe Yehova sanachotse mkwiyo wake woopsa, umene anali nawo
pa Yuda chifukwa cha zonse zimene anachita Manase poputa mkwiyo
wa Mulungu. 27 Choncho Yehova anati, "Ndidzawachotsanso anthu a ku
Yuda pamaso panga monga ndinachotsera anthu a ku Israeli ndipo ndidza-
wukana mzinda wa Yerusalemu, mzinda umene ndinawusankha, pamodzi
ndi Nyumba ino imene ndinati, 'Dzina langa lidzakhala m'menemo.' "

28 Ntchito zina za Yosiya ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda?

29 Yosiya akanali mfumu, Farao wotchedwa Neko, mfumu ya Igupto,
anapita ku Mtsinje wa Yufurate kukathandiza mfumu ya ku Asiriya.
Mfumu Yosiya anapita kukachita naye nkhondo, koma Neko anakumana
naye ndi kumupha ku Megido. 30 Atumiki a Yosiyayo ananyamula
mtembo wake mu galeta kuchokera ku Megido mpaka ku Yerusalemu
ndipo anamuyika m'manda akeake. Ndipo anthu a m'dzikomo anatenga
Yehowahazi mwana wa Yosiya namudzoza, ndipo iye analowa ufumu
m'malo mwa abambo ake.

### *Yehowahazi Mfumu ya Yuda*

31 Yehowahazi anakhala mfumu ali ndi 23 ndipo analamulira mu
Yerusalemu miyezi itatu. Amayi ake anali Hamutali, mwana wa Yeremiya
wa ku Libina. 32 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova monga momwe
anachitira makolo ake. 33 Farao Neko anamuyika m'ndende ku Ribula
m'dziko la Hamati kuti asalamulirenso mu Yerusalemu. Farao analamula
Yuda kuti azikhoma msonkho wa siliva wolemera makilogalamu 3,400,
ndiponso golide wolemera makilogalamu 34. 34 Farao Neko anayika
Eliyakimu mwana wa Yosiya kuti akhale mfumu m'malo mwa abambo
ake Yosiya, ndipo anasintha dzina lake kukhala Yehoyakimu. Koma iye
anatenga Yehowahazi kupita naye ku Igupto ndipo anakafera kumeneko.
35 Yehoyakimu anapereka kwa Farao Neko siliva ndi golide amene ana-
mufuna uja. Koma kuti iye apereke zimenezi, amankhometsa msonkho
m'dziko mwakemo ndipo amalandira siliva ndi golide kuchokera kwa
anthu a m'dzikomo molingana ndi chuma cha munthu aliyense.

### *Yehoyakimu Mfumu ya Yuda*

36 Yehoyakimu anali wa zaka 25 pamene anakhala mfumu ndipo
analamulira mu Yerusalemu zaka 11. Amayi ake anali Zebuda, mwana
wa Pedaya wa ku Ruma. 37 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova monga
momwe anachitira makolo ake.

## 24

1 Pa nthawi ya ulamuliro wa Yehoyakimu, Nebukadinezara mfumu
ya Babuloni anadzathira nkhondo dzikolo ndipo Yehoyakimu anakhala
pansi pa ulamuliro wake zaka zitatu. Koma kenaka anasintha maganizo

ake nawukira Nebukadinezara. 2 Yehova anatumiza magulu a Ababu-
loni, Aaramu, Amowabu ndi Aamoni, kudzathira nkhondo Yuda. Iye
anawatumiza kudzawononga Yuda molingana ndi mawu amene Yehova
ananeneratu kudzera mwa aneneri ake. 3 Ndithu, izi zinachitikira
Yuda monga momwe Yehova analamulira n'cholinga choti awachotse
pamaso pake chifukwa cha machimo a Manase ndi zonse zimene
anachita, 4 kuphatikizapo kukhetsa magazi a anthu osalakwa. Chifukwa
iye anadzaza Yerusalemu ndi magazi a anthu osalakwa ndipo Yehova
sanafune kumukhululukira.
5 Ntchito zina za Yehoyakimu ndi zonse zimene anachita, kodi sizinalem-
bedwe m'buku la mbiri ya mafumu a Yuda? 6 Yehoyakimu anamwalira
ndipo anayikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake. Ndipo Yehoyakini
mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.
7 Mfumu ya Igupto sinatulukenso m'dziko lake chifukwa mfumu ya
Babuloni inalanda mayiko onse kuchokera ku Mtsinje wa ku Igupto mpaka
ku Mtsinje wa Yufurate.

### *Yoyakini Mfumu ya Yuda*

8 Yehoyakini anakhala mfumu ali ndi zaka 18 ndipo analamulira mu
Yerusalemu miyezi itatu. Amayi ake anali Nehusita mwana wa Elinatani
wa ku Yerusalemu. 9 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova monga
anachitira abambo ake.
10 Nthawi imeneyo ankhondo a Nebukadinezara mfumu ya Babuloni
anabwera ku Yerusalemu nazinga mzindawo ndi misasa ya nkhondo
11 ndipo Nebukadinezara anafika ku mzindawo pamene ankhondo ake
anawuzinga. 12 Yehoyakini mfumu ya Yuda pamodzi ndi amayi ake, atu-
miki ake, anthu ake olemekezeka ndiponso akuluakulu onse anadzipereka
kwa mfumu ya ku Babuloni.
Mfumu ya Babuloni inagwira Yoyakini ukapolo m'chaka chachisanu ndi
chitatu cha ufumu wake. 13 Monga ananenera Yehova, Nebukadinezara
anachotsa chuma chonse cha m'Nyumba ya Yehova ndiponso cha
m'nyumba ya mfumu ndipo anatenga ziwiya zonse zagolide za ku Nyumba
ya Yehova zimene Solomoni mfumu ya Israeli anapanga. 14 Anatenga
anthu onse a mu Yerusalemu kupita nawo ku ukapolo. Akuluakulu onse
pamodzi ndi anthu ankhondo, anthu onse aluso ndi amisiri osula onse
pamodzi analipo 10,000. Osauka okha ndiye anatsala m'dzikomo.
15 Nebukadinezara anatenga Yehoyakini ngati kapolo kupita naye ku
Babuloni. Mu Yerusalemu anatenganso amayi a mfumu, akazi ake,
akuluakulu ake ndiponso anthu olemekezeka m'dzikomo. 16 Mfumu
ya Babuloni inatumizanso ku Babuloni anthu ankhondo 70,000, anthu
amphamvu ndi okonzeka kupita ku nkhondo, anthu aluso ndi amisiri
osula 1,000. 17 Iye analonga ufumu Mataniya, malume wa Yoyakini m'malo
mwake ndipo anasintha dzina lake kuti akhale Zedekiya.

### *Zedekiya Mfumu ya Yuda*

18 Zedekiya anakhala mfumu ali ndi zaka 21 ndipo analamulira mu
Yerusalemu zaka 11. Amayi ake anali Hamutali mwana wa Yeremiya wa
ku Libina. 19 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova monga anachitira
Yehoyakimu. 20 Zonsezi zinachitikira Yerusalemu ndi Yuda chifukwa cha
mkwiyo wa Mulungu ndipo pa mapeto pake anawachotsa pamaso pake.

### *Kuwonongeka kwa Yerusalemu*

Ndipo Zedekiya anawukira mfumu ya Babuloni.

# 25

1 Choncho m'chaka chachisanu ndi chinayi cha ulamuliro wa Zedekiya,
mwezi wakhumi, pa tsiku lakhumi la mwezi, Nebukadinezara mfumu ya
Babuloni anabwera ndi gulu lake lonse la ankhondo, nadzathira nkhondo
mzinda wa Yerusalemu. Iye anamanga misasa kunja kwa mzindawo ndipo
anamanga mitumbira ya nkhondo kuzungulira mzindawo. 2 Mzindawo
anawuzinga mpaka chaka cha khumi ndi chimodzi cha Mfumu Zedekiya.
3 Pa tsiku lachisanu ndi chinayi pa mwezi wachinayi, njala inakula
kwambiri mu mzindamo kotero kuti anthu analibe chakudya. 4 Pamenepo
khoma la mzindawo linabowoledwa ndipo gulu lonse la ankhondo
linathawa usiku kudzera pa chipata cha pakati pa makoma awiri pafupi
ndi munda wa mfumu, ngakhale kuti Ababuloni anali atazinga mzindawo.
Iwo anathawira cha ku Araba, 5 koma gulu la ankhondo la ku Babuloni
linalondola mfumu Zedekiya ndi kumupeza m'chigwa cha ku Yeriko.
Ankhondo onse anamusiya yekha nabalalika. 6 Anagwidwa napita naye
kwa mfumu ya ku Babuloni ku Ribula, kumene anagamula mlandu
wa Zedekiyayo. 7 Iwo anapha ana a Zedekiya iyeyo akuona. Kenaka
anakolowola maso a Zedekiya namumanga ndi unyolo wamkuwa ndi
kupita naye ku Babuloni.

8 Mwezi wachisanu, pa tsiku lachisanu ndi chiwiri la mwezi, m'chaka
cha 19 cha Nebukadinezara, mfumu ya Babuloni, Nebuzaradani, mkulu
wa asilikali oteteza mfumu, nduna ya mfumu ya Babuloni, anabwera
ku Yerusalemu. 9 Iye anatentha Nyumba ya Yehova, nyumba ya mfumu
pamodzi ndi nyumba zonse za mu Yerusalemu. Anatentha nyumba
iliyonse yofunika. 10 Gulu lonse la ankhondo la ku Babuloni limene
linali ndi mkulu wa asilikali oteteza mfumu ija, linagumula malinga
ozungulira Yerusalemu. 11 Nebuzaradani mkulu wa asilikali uja anatenga
anthu amene anatsala mu mzindamo, ndi ena amene anathawira kwa
mfumu ya Babuloni, pamodzi ndi ena onse kupita nawo ku ukapolo
ku Babuloni. 12 Koma mkulu wa asilikaliyo anasiya anthu ena osauka
kwambiri m'dzikomo kuti azisamalira minda ya mpesa ndi minda ina.

13 Ababuloni anaphwanya zipilala zamkuwa, maphaka ndiponso mbiya
ya mkuwa zimene zinali m'Nyumba ya Yehova ndipo anatenga mkuwawo
napita nawo ku Babuloni. 14 Iwo anatenganso miphika, mafosholo,
mbaniro za nyale, mbale ndi ziwiya zonse zamkuwa zimene ankagwiritsa
ntchito potumikira m'Nyumbayo. 15 Mkulu wa asilikali uja anatenganso
zofukizira lubani ndi mbale zowazira magazi. Zonsezi zinali zopangidwa
ndi golide wabwino kwambiri kapena siliva.

16 Mkuwa wochokera ku zipilala ziwiri zija, mbiya ija ndi maphaka
aja, zimene Solomoni anapanga m'Nyumba ya Yehova, kuchuluka kwake
kunali kosawerengeka. 17 Chipilala chilichonse chinali chotalika mamita
asanu ndi atatu. Mutu wa mkuwa umene unali pamwamba pa chipilala-
cho unali mita imodzi ndi theka ndipo unakongoletsedwa ndi ukonde wa
makangadza a mkuwa amene anazungulira mutuwo. Chipilala chachiwiri
chinali chofanana ndi chinacho, ndipo chinali ndi ukonde.

18 Mkulu wa asilikali uja anagwira ukapolo mkulu wa ansembe Seraya,
Zefaniya wachiwiri wa mkulu wa ansembe ndi alonda atatu apakhomo.
19 Mwa anthu amene anali mu mzindamo, anatenga mkulu amene
ankalamulira ankhondo ndiponso alangizi asanu a mfumu. Anatenganso
mlembi wa mtsogoleri wa ankhondo amene ankalemba anthu ntchito ya
usilikali m'dzikomo pamodzi ndi anthu ake 60 amene anali mu mzindamo.

[20] Nebuzaradani mkulu wa asilikali uja anawatenga onsewo napita nawo
kwa mfumu ya Babuloni ku Ribula. [21] Ku Ribulako, m'dziko la Hamati,
mfumu ya ku Babuloni inalamula kuti awakwapule ndi kuwapha.
Choncho Ayuda anatengedwa ukapolo kuwachotsa m'dziko lawo.
[22] Nebukadinezara mfumu ya Babuloni anasankha Gedaliya mwana wa
Ahikamu, mwana wa Safani, kukhala woyang'anira anthu amene anatsala
ku Yuda. [23] Atsogoleri onse ankhondo ndi anthu awo atamva kuti mfumu
ya Babuloni yasankha Gedaliya kukhala bwanamkubwa, anabwera kwa
Gedaliya ku Mizipa. Atsogoleriwo mayina awo anali awa: Ismaeli mwana
wa Netaniya, Yohanani mwana wa Kareya, Seraya mwana wa Tanihumeti
wa ku Netofa ndi Yaazaniya mwana wa Maakati, pamodzi ndi anthu awo.
[24] Gedaliya analumbira powatsimikizira iwo ndi anthu awo. Iye anati,
"Musachite mantha ndi atsogoleri Ababuloniwa. Khalani m'dziko muno
ndipo tumikirani mfumu ya Babuloni. Mukatero zinthu zidzakuyenderani
bwino."
[25] Koma pa mwezi wachisanu ndi chiwiri, Ismaeli mwana wa Netaniya,
mwana wa Elisama, wa banja laufumu, anabwera ndi anthu khumi
ndipo anapha Gedaliya pamodzi ndi Ayuda ndi anthu a ku Babuloni
amene anali naye limodzi ku Mizipa. [26] Chifukwa cha zimenezi, anthu
onse kuyambira wamng'ono mpaka wamkulu, pamodzi ndi atsogoleri a
ankhondo anathawira ku Igupto chifukwa choopa Ababuloni.

### *Kumasulidwa kwa Yehoyakini*

[27] Pa chaka cha 37 cha ukapolo wa Yehoyakini mfumu ya Yuda,
chaka chimene Evili-Merodaki anakhala mfumu ya Babuloni, anamasula
Yehoyakini m'ndende pa mwezi wa 12 pa tsiku la 27. [28] Anamukomera
mtima namukweza kupambana mafumu ena onse amene anali naye ku
Babuloni. [29] Choncho Yoyakini anavula zovala zake za ku ndende, ndipo
ankadya ndi mfumu masiku onse a moyo wake. [30] Mfumu inkamupatsa
Yehoyakini chakudya tsiku lililonse pa moyo wake wonse.

# 1 Mbiri

*Mbiri ya Makolo Kuchokera pa Adamu Mpaka pa Abrahamu*

*Mpaka pa Ana a Nowa*

1 Adamu, Seti, Enosi 2 Kenani, Mahalaleli, Yaredi, 3 Enoki, Metusela,
Lameki, Nowa.

4 Ana a Nowa,
Semu, Hamu ndi Yafeti.

*Fuko la Yafeti*

5 Ana aamuna a Yafeti anali:
Gomeri, Magogi, Madai, Yavani, Tubala, Mesaki ndi Tirasi.
6 Ana aamuna a Gomeri anali:
Asikenazi, Rifati ndi Togarima
7 Ana aamuna a Yavani anali:
Elisa, Tarisisi, Kitimu ndi Rodanimu.

*Fuko la Hamu*

8 Ana aamuna a Hamu anali:
Kusi, Miziraimu, Puti ndi Kanaani
9 Ana aamuna a Kusi anali:
Seba, Havila, Sabita, Raama ndi Sabiteka
Ana aamuna a Raama anali:
Seba ndi Dedani.
10 Kusi anali abambo a Nimurodi amene anali wankhondo wamphamvu kwambiri pa dziko lapansi.
11 Igupto ndiye kholo la
Aludi, Aanami, Alehabu, Anafutu, 12 Apaturusi, Akasilu (kumene
kunachokera Afilisti) ndi Akafitori.
13 Kanaani anabereka mwana wake wachisamba Sidoni,
ndipo anaberekanso Ahiti, 14 Ayebusi, Aamori, Agirigasi 15 Ahivi,
Aariki, Asini 16 Aaravadi, Azemari ndi Ahamati.

*Fuko la Semu*

17 Ana aamuna a Semu anali:
Elamu, Asuri, Aripakisadi, Ludi ndi Aramu.
Ana aamuna a Aramu anali:
Uzi, Huri, Geteri ndi Mesaki.
18 Aripakisadi anabereka Sela
ndipo Selayo anabereka Eberi:
19 Eberi anabereka ana aamuna awiri:
wina anamutcha Pelegi, chifukwa pa nthawiyo anthu a pa dziko lapansi anagawikana. Dzina la m'bale wake linali Yokitani.
20 Yokitani anabereka
Alimodadi, Selefi, Hazari-Maveti, Yera, 21 Hadoramu, Uzali, Dikila
22 Obali, Abimaeli, Seba, 23 Ofiri, Havila ndi Yobabu. Onsewa anali
ana aamuna a Yokitani.

24 Semu, Aripakisadi, Sela
25 Eberi, Pelegi, Reu

26 Serugi, Nahori, Tera
27 ndi Abramu (amene ndi Abrahamu).

### *Banja la Abrahamu*

28 Ana a Abrahamu ndi awa:
Isake ndi Ismaeli.

### *Zidzukulu za Hagara*

29 Zidzukulu zake zinali izi:
Nebayoti ndiye anali mwana woyamba wa Ismaeli, kenaka Kedara,
Adibeeli, Mibisamu, 30 Misima, Duma, Masa, Hadadi, Tema, 31 Yeturi,
Nafisi ndi Kedema. Awa anali ana a Ismaeli.

### *Zidzukulu za Ketura*

32 Ana a Ketura mzikazi wa Abrahamu anali awa:
Zimurani, Yokisani, Medani, Midiyani, Isibaki ndi Suwa.
Ana a Yokisani ndi awa:
Seba ndi Dedani
33 Ana aamuna a Midiyani anali,
Efai, Eferi, Hanoki, Abida ndi Elida.
Onsewa anali zidzukulu za Ketura.

### *Zidzukulu za Sara*

34 Abrahamu anabereka Isake.
Ana a Isake anali awa:
Esau ndi Israeli.

### *Ana a Esau*

35 Ana aamuna a Esau anali awa:
Elifazi, Reueli, Yeusi, Yolamu ndi Kora.
36 Ana a Elifazi anali awa:
Temani, Omari, Zefo, Gatamu ndi Kenazi:
Amene anabereka ndi Timna: Amaleki.
37 Ana a Reueli anali awa:
Nahati, Zera, Sama ndi Miza.

### *Anthu a ku Seiri ku Edomu*

38 Ana a Seiri anali awa:
Lotani, Sobala, Zibeoni, Ana, Disoni, Ezeri ndi Disani.
39 Ana aamuna a Lotani anali awa:
Hori ndi Homamu. Timna anali mlongo wake wa Lotani.
40 Ana aamuna a Sobala anali awa:
Alivani, Manahati, Ebala, Sefo ndi Onamu.
Ana aamuna a Zibeoni anali awa:
Ayiwa ndi Ana.
41 Mwana wa Ana anali
Disoni.
Ana a Disoni anali awa:
Hemudani, Esibani, Itirani ndi Kerani
42 Ana aamuna a Ezeri anali awa:
Bilihani, Zaavani ndi Yaakani.
Ana aamuna a Disani anali awa:
Uzi ndi Arani.

### *Mafumu a ku Edomu*

43 Awa ndi mafumu amene ankalamulira dziko la Edomu, mfumu
iliyonse ya Israeli isanayambe kulamulira kumeneko:

Bela mwana wa Beori, mzinda wake ankawutcha Dinihaba.
44 Bela atamwalira, Yobabu mwana wa Zera wochokera ku Bozira
analowa ufumu m'malo mwake.
45 Yobabu atamwalira, Husamu wochokera ku dziko la Atemani, analowa
ufumu m'malo mwake.
46 Husamu atamwalira, Hadadi mwana wa Bedadi, amene anagonjetsa
Amidiyani m'dziko la Mowabu, analowa ufumu m'malo mwake.
Mzinda wake unkatchedwa Aviti.
47 Hadadi atamwalira, Samila wochokera ku Masireka analowa ufumu
m'malo mwake.
48 Samila atamwalira, Sauli wochokera ku Rehoboti wa ku Mtsinje
analowa ufumu m'malo mwake.
49 Sauli atamwalira, Baala-Hanani mwana wa Akibori analowa ufumu
m'malo mwake.
50 Pamene Baala-Hanani anamwalira, Hadadi analowa ufumu m'malo
mwake. Mzinda wake unkatchedwa Pau, ndipo dzina la mkazi wake
linali Mehatabeli mwana wa Matiredi, mwana wamkazi wa Me-
Zahabu. 51 Hadadi anamwaliranso.

Mafumu a ku Edomu anali:
Timna, Aliva, Yeteti, 52 Oholibama, Ela, Pinoni, 53 Kenazi, Temani,
Mibezari, 54 Magidieli ndi Iramu. Awa anali mafumu a ku Edomu.

# 2

### *Ana a Israeli*

1 Ana a Israeli anali awa:
Rubeni, Simeoni, Levi, Yuda, Isakara, Zebuloni, 2 Dani, Yosefe,
Benjamini, Nafutali, Gadi ndi Aseri.

### *Yuda Mpaka pa Ana a Hezironi*

### *Ana a Hezironi*

3 Ana a Yuda anali awa:
Eri, Onani ndi Sela. Ana atatu awa anabereka ndi mkazi wa
Chikanaani, Batisuwa. Eri, mwana woyamba wa Yuda anali woyipa
kwambiri pamaso pa Yehova, kotero Yehova anamupha. 4 Mpongozi
wake Tamara anamuberekera Perezi ndi Zera. Ana onse a Yuda
analipo asanu.

5 Ana a Perezi anali awa:
Hezironi ndi Hamuli.
6 Ana a Zera anali awa:
Zimuri, Etani, Hemani, Kalikoli ndi Dara. Onse analipo asanu.
7 Mwana wa Karimi anali
Akani, amene anabweretsa mavuto pakati pa Israeli pamene anatenga
zinthu zoyenera kuwonongedwa.
8 Mwana wa Etani anali
Azariya.
9 Ana amene anabadwa kwa Hezironi anali:
Yerahimeeli, Ramu ndi Kelubai.

### *Kuchokera kwa Ramu Mwana wa Hezironi*

10 Ramu anabereka

Aminadabu ndipo Aminadabu anali abambo ake a Naasoni, mtsogoleri
wa fuko la Yuda. 11 Naasoni anabereka Salima, Salima anabereka
Bowazi, 12 Bowazi anabereka Obedi ndipo Obedi anabereka Yese.
13 Yese anabereka
Eliabu mwana wake woyamba, wachiwiri Abinadabu, wachitatu
Simea, 14 wachinayi Netaneli, wachisanu Radai, 15 wachisanu ndi
chimodzi Ozemu ndi wachisanu ndi chiwiri Davide. 16 Alongo awo
anali Zeruya ndi Abigayeli. Ana atatu a Zeruya anali Abisai Yowabu
ndi Asaheli. 17 Abigayeli anali amayi ake a Amasa amene abambo
ake anali Yeteri wa fuko la Ismaeli.

### *Kalebe Mwana wa Hezironi*

18 Kalebe mwana wa Hezironi anabereka ana mwa Azuba mkazi wake
(ndi mwa Yerioti). Ana a mkaziyo anali awa: Yeseri, Sobabu ndi
Aridoni. 19 Azuba atamwalira, Kalebe anakwatira Efurata, amene
anamuberekera Huri. 20 Huri anabereka Uri ndipo Uri anabereka
Bezaleli.
21 Patapita nthawi, Hezironi anagona ndi mwana wamkazi wa Makiri
abambo ake a Giliyadi (iye anamukwatira ali ndi zaka 60) ndipo
anamuberekera Segubu. 22 Segubu anabereka Yairi, amene anali
ndi mizinda 23 ku Giliyadi. 23 (Koma Gesuri ndi Aramu analanda
Havoti Yairi komanso Kenati ndi madera ake onse ozungulira, mizinda
makumi asanu ndi umodzi). Onsewa anali adzukulu, a Makiri abambo
ake a Giliyadi.

24 Atamwalira Hezironi ku Kalebe Efurata, Abiya mkazi wa Hezironi
anamuberekera Asihuri abambo a Tekowa.

### *Yerahimeeli Mwana wa Hezironi*

25 Ana a Yerahimeeli, mwana woyamba wa Hezironi anali:
Ramu, mwana wake woyamba, Buna, Oreni, Ozemu ndi Ahiya.
26 Yerahimeeli anali ndi mkazi wina amene dzina lake linali Atara,
amene anali amayi a Onamu.
27 Ana a Ramu, mwana woyamba wa Yerahimeeli, anali awa:
Maazi, Yamini ndi Ekeri.
28 Ana a Onamu anali awa:
Shamai ndi Yada.
Ana a Shamai anali awa:
Nadabu ndi Abisuri.
29 Mkazi wa Abisuri anali Abihaili, amene anamuberekera Ahibani ndi
Molidi.
30 Ana a Nadabu anali awa:
Seledi ndi Apaimu. Koma Seledi anamwalira wopanda ana.
31 Ana a Apaimu anali awa:
Isi, amene anabereka Sesani.
Sesani anabereka Ahilai.
32 Ana a Yada, m'bale wa Samai, anali awa:
Yereri ndi Yonatani. Koma Yeteri anamwalira wopanda ana.
33 Ana a Yonatani anali awa:
Peleti ndi Zaza.
Amenewa anali adzukulu a Yerahimeeli.
34 Sesani sanabereke ana aamuna koma aakazi okhaokha.

Iye anali ndi wantchito wa ku Igupto, dzina lake Yariha. 35 Sesani
anapereka mwana wake wamkazi kwa Yariha wantchito wake kuti
amukwatire ndipo anamuberekera Atayi.

36 Atayi anali abambo ake a Natani,
Natani anali abambo ake a Zabadi,
37 Zabadi anali abambo a Efilali,
Efilali anali abambo a Obedi,
38 Obedi anali abambo a Yehu,
Yehu anali abambo a Azariya,
39 Azariya anali abambo a Helezi,
Helezi anali abambo a Eleasa,
40 Eleasa anali abambo ake a Sisimai,
Sisimai anali abambo a Salumu,
41 Salumu anali abambo a Yekamiya,
Yekamiya anali abambo a Elisama.

### *Mabanja a Kalebe*

42 Ana a Kalebe m'bale wa Yerahimeeli anali awa:
Mesa mwana wachisamba, anali abambo a Zifi, ndipo mwana wake
Maresa anali abambo a Hebroni.
43 Ana a Hebroni anali awa:
Kora, Tapuwa, Rekemu ndi Sema. 44 Sema anali abambo ake Rahamu
ndipo Rahamu anali abambo a Yorikeamu. Rekemu anali abambo a
Samai. 45 Mwana wa Samai anali Maoni, ndipo Maoni anali abambo
a Beti Zuri.
46 Efai, mzikazi wa Kalebe, anali amayi a Harani, Moza ndi Gazezi.
Harani anali abambo a Gazezi.
47 Ana a Yahidai anali awa:
Regemu, Yotamu, Gesani, Peleti, Efai ndi Saafi.
48 Maaka mzikazi wa Kalebe anali mayi Seberi ndi Tirihana. 49 Iye an-
aberekanso Saafi abambo a Madimena ndi Seva abambo a Makibena
ndi Gibeya. Mwana wamkazi wa Kalebe anali Akisa. 50 Izi zinali
zidzukulu za Kalebe.

Ana a Huri mwana wachisamba wa Efurata anali awa:
Sobala abambo a Kiriati Yearimu, 51 Salima abambo a Betelehemu ndi
Harefu abambo ake a Beti-Gadera.
52 Zidzukulu za Sobala abambo a Kiriati Yearimu zinali izi:
Harowe, theka la banja la Manahati, 53 ndipo mabanja a Kiriati-
Yeyarimu anali awa: Aitiri, Aputi, Asumati ndi Amisirai. Azorati
ndi Aesitaoli anachokera kwa amenewa.
54 Zidzukulu za Salima zinali izi:
Betelehemu, Anetofati, Atiroti-Beti-Yowabu, theka la banja la Man-
ahati, Azori, 55 ndiponso mabanja a alembi amene amakhala ku
Yabesi: Atiroti, Asimeati ndiponso Asukati. Awa ndi Akeni amene
anachokera kwa Hamati, kholo la Arekabu.

## 3

### *Ana a Davide*

1 Ana aamuna a Davide amene anabadwira ku Hebroni anali awa:
Woyamba anali Amnoni, amayi ake anali Ahinoamu wa ku Yezireeli;
wachiwiri anali Danieli, amayi ake anali Abigayeli wa ku Karimeli;

2 wachitatu anali Abisalomu, mwana wa Maaka mwana wa Talimai mfumu ya Gesuri;
wachinayi anali Adoniya amayi ake anali Hagiti;
3 wachisanu anali Sefatiya, amayi ake anali Abitali;
wachisanu ndi chimodzi anali Itireamu, amayi ake anali Egila.
4 Ana asanu ndi mmodzi awa a Davide anabadwira ku Hebroni kumene analamulirako zaka zisanu ndi ziwiri ndi miyezi isanu ndi umodzi.
Davide analamuliranso mu Yerusalemu kwa zaka 33,
5 ndipo ana amene anabadwira ku Yerusalemuko anali awa:
Samua, Sobabu, Natani ndi Solomoni. Ana anayi awa anali a Batisuwa mwana wa Amieli.
6 Anaberekanso Ibihari, Elisua, Elipeleti,
7 Noga, Nefegi, Yafiya,
8 Elisama, Eliada ndi Elifeleti, onse analipo asanu ndi anayi.
9 Onsewa anali ana a Davide, osawerengera ana a azikazi. Ndipo mlongo wawo anali Tamara.

### *Mafumu a Yuda*

10 Mwana wa Solomoni anali Rehabiamu,
Rehabiamu anabereka Abiya,
Abiya anabereka Asa,
Asa anabereka Yehosafati,
11 Yehosafati anabereka Yehoramu,
Yehoramu anabereka Ahaziya,
Ahaziya anabereka Yowasi,
12 Yowasi anabereka Amaziya,
Amaziya anabereka Azariya,
Azariya anabereka Yotamu,
13 Yotamu anabereka Ahazi,
Ahazi anabereka Hezekiya,
Hezekiya anabereka Manase,
14 Manase anabereka Amoni,
Amoni anabereka Yosiya.
15 Ana a Yosiya anali awa:
Yohanani mwana wake woyamba,
Yehoyakimu mwana wake wachiwiri,
Zedekiya mwana wake wachitatu,
Salumu mwana wake wachinayi.
16 Ana a Yehoyakimu:
Yekoniya
ndi Zedekiya mwana wake.

### *Mayina a Mafumu Utatha Ukapolo*

17 Zidzukulu za Yekoniya wa m'ndende zinali izi:
mwana wake Silatieli,
18 Malikiramu, Pedaya, Senazara, Yekamiya, Hosama ndi Nedabiya.
19 Ana a Pedaya anali awa:
Zerubabeli ndi Simei.
Ana a Zerubabeli anali awa:
Mesulamu ndi Hananiya.
Mlongo wawo anali Selomiti.
20 Panalinso ana ena asanu awa:
Hasubu, Oheli, Berekiya, Hasabiya ndi Yusabu-Hesedi.
21 Zidzukulu za Hananiya zinali izi:

Pelatiya ndi Yesaiya, ndiponso ana a Refaya, ana a Arinani, ana a Obadiya ndi ana a Sekaniya.
22 Zidzukulu za Sekaniya zinali izi:
Semaya ndi ana ake:
Hatusi, Igala, Bariya, Neariya ndi Safati. Onse anali asanu ndi mmodzi.
23 Ana a Neariya anali awa:
Eliyoenai, Hezekiya ndi Azirikamu. Onse anali atatu.
24 Ana a Eliyoenai: Hodaviya, Eliyasibu, Pelaya, Akubu,
Yohanani, Delaya ndi Anani, onse anali asanu ndi awiri.

# 4

*Mabanja Ena a Yuda*
1 Ana a Yuda anali awa:
Perezi, Hezironi, Karimi, Huri ndi Sobali.
2 Reaya mwana wa Sobala anabereka Yahati, ndipo Yahati anabereka Ahumai ndi Lahadi. Awa anali mabanja a Azorati.
3 Ana a Etamu anali awa:
Yezireeli, Isima ndi Idibasi. Dzina la mlongo wawo linali Hazeleliponi.
4 Penueli anabereka Gedori, ndipo Ezeri anabereka Husa.
Awa anali ana a Huri, mwana wachisamba wa Efurata ndi abambo a Betelehemu.
5 Asihuri abambo a Tekowa anali ndi akazi awiri, Hela ndi Naara.
6 Naara anamuberekera Ahuzamu, Heferi, Temani ndi Haahasitari. Awa ndiwo anali ana a Naara.
7 Ana a Hela:
Zereti, Zohari, Etinani, 8 ndi Kozi, amene anali abambo ake a Anubi ndi Hazo-Beba ndi mabanja a Ahariheli mwana wa Harumi.

9 Yabesi anali munthu wolemekezeka kwambiri kuposa abale ake.
Amayi ake anamutcha Yabesi kutanthauza kuti, "Chifukwa ndinamubala
ndi ululu wambiri." 10 Yabesi analira kwa Mulungu wa Israeli kuti,
"Mundidalitse ndipo mukulitse dziko langa! Dzanja lanu likhale pa ine
ndipo mundisunge kuti choyipa chisandigwere ndi kundisautsa." Ndipo
Mulungu anamupatsa chopempha chakecho.

11 Kelubi, m'bale wa Suha, anabereka Mehiri, amene anabereka Esitoni.
12 Esitoni anabereka Beti-Rafa, Paseya ndi Tehina amene anabereka Iri Nahasi. Amenewa ndiwo anthu a ku Reka.

13 Ana a Kenazi anali awa:
Otanieli ndi Seraya.
Ana a Otanieli anali awa:
Hatati ndi Meonotai. 14 Meonotai anabereka Ofura.
Seraya anabereka Yowabu,
amene anabereka Ge-Harasimu. Anawatcha dzina ili chifukwa anthu ake anali amisiri.
15 Ana a Kalebe mwana wa Yefune anali awa:
Iru, Ela ndi Naama.
Mwana wa Ela anali
Kenazi.
16 Ana a Yehaleleli anali awa:
Zifi, Zifa, Tiriya ndi Asareli.

17 Ana a Ezara anali awa:
Yeteri, Meredi, Eferi ndi Yaloni. Mmodzi mwa akazi a Meredi anabereka Miriamu, Samai ndi Isiba abambo ake a Esitemowa.
18 (Mkazi wake wa Chiyuda anabereka Yaredi abambo ake a Gedori, Heberi abambo ake a Soko ndi Yekutieli abambo a Zanowa). Awa anali ana a mwana wamkazi wa Farao, Bitia, amene Meredi anakwatira.
19 Ana a mkazi wa Hodiya, mlongo wa Nahamu anali awa:
abambo ake a Keila wa ku Garimi ndi Esitemowa wa ku Maaka.
20 Ana a Simeoni anali awa:
Amnoni, Rina, Beni-Hanani ndi Tiloni.
Ana a Isi anali awa:
Zoheti ndi Beni-Zoheti.
21 Ana a Sela mwana wa Yuda anali awa:
Eri amene anabereka Leka, Laada amene anabereka Maresa ndi mabanja a anthu owomba nsalu zofewa ndi zosalala a ku Beti-
Asibeya, 22 Yokimu, anthu a ku Kozeba, ndiponso Yowasi ndi Sarafi, amene ankalamulira Mowabu ndi Yasibu-Lehemu. (Nkhani zimenezi ndi zakalekale).
23 Iwo anali owumba mbiya amene ankakhala ku Netaimu ndi Gederi. Ankakhala kumeneko ndi kumatumikira mfumu.

### *Simeoni*

24 Ana a Simeoni anali awa:
Nemueli, Yamini, Yaribu, Zera ndi Sauli;
25 Salumu anali mwana wa Sauli, Mibisamu anali mwana wa Salumu ndipo Misima anali mwana wa Mibisamu.
26 Zidzukulu za Misima zinali izi:
Hamueli, Zakuri ndi Simei.
27 Simei anali ndi ana aamuna 16 ndi ana aakazi 6, koma abale ake sanabereke ana ambiri; kotero banja lawo silinakule ngati anthu ena a ku
Yuda. 28 Iwo amakhala ku Beeriseba, Molada, Hazari-Suwali, 29 Biliha,
Ezemu, Toladi, 30 Betueli, Horima, Zikilagi, 31 Beti-Marikaboti, Hazari-Susimu, Beti-Biri ndi Saaraimu. Iyi inali mizinda yawo mpaka pa nthawi
ya ulamuliro wa Davide. 32 Midzi yowazungulira inali Etamu, Aini, Rimoni,
Tokeni ndi Asani, midzi isanu 33 ndi midzi yonse yozungulira mizinda imeneyi mpaka ku Baala. Awa anali malo awo okhalapo. Ndipo anasunga mbiri ya makolo awo.

34 Mesobabu, Yamuleki, Yosa mwana wa Amaziya, 35 Yoweli, Yehu
mwana wa Yosibiya, mwana wa Seraya, mwana wa Asieli, 36 komanso
Eliyoenai, Yaakoba, Yesohaya, Asaya, Adieli, Yesimieli, Benaya,
37 ndiponso Ziza mwana wa Sifi, mwana wa Aloni, mwana wa Yedaya, mwana wa Simiri, mwana wa Semaya.

38 Anthu amene atchulidwawa anali atsogoleri a mabanja awo. Mabanja
awo anakula kwambiri 39 ndipo anakafika ku malire a Gedori ku chigwa
cha kummawa kufuna msipu wodyetsa ziweto zawo. 40 Anapeza msipu
wobiriwira ndi wabwino ndipo dziko linali lalikulu, la mtendere ndi bata. Kumeneko kunkakhala fuko la Hamu poyamba.
41 Anthu amene mayina awowa alembedwa, anabwera pa nthawi ya Hezekiya mfumu ya Yuda. Iwo anathira nkhondo fuko la Hamu m'malo awo amene amakhala komanso Ameuni amene anali kumeneko ndipo

anawononga onsewo kotero kuti mbiri yawo simvekanso mpaka lero lino.
Kotero iwo anakhala m'malo awo chifukwa kunali msipu wa ziweto zawo.
42 Ndipo anthu 500 a fuko la Simeoni, motsogozedwa ndi Pelatiya, Neariya,
Refaya ndi Uzieli, ana a Isi, analanda dziko lamapiri la Seiri. 43 Iwo anapha
Aamaleki otsala amene anali atapulumuka ndipo akukhala kumeneko
mpaka lero lino.

# 5

*Fuko la Rubeni*

1 Ana a Rubeni mwana woyamba wa Israeli (iye anali woyamba
kubadwa, koma atagona ndi mkazi wamng'ono wa abambo ake, ulemu
wake wokhala mwana woyamba unaperekedwa kwa ana a Yosefe. Kotero
iye sanalembedwe pa mndandanda wa mayina ngati mwana woyamba
kubadwa, 2 ndipo ngakhalenso Yuda anali wamphamvu kwambiri pakati
pa abale ake, ndi kuti wolamulira anachokera mwa iye, ulemu wa mwana
woyamba kubadwa unaperekedwa kwa Yosefe) 3 ana a Rubeni mwana
woyamba wa Israeli ndi awa:

Hanoki, Palu, Hezironi, ndi Karimi.

4 Ana a Yoweli anali awa:

Semaya, Gogi,
Simei, 5 Mika,
Reaya, Baala,
6 ndiponso Beeri, amene Tigilati-Pileseri mfumu ya Asuri anamugwira ukapolo. Mtsogoleri wa fuko la Rubeni anali Beeri.

7 Abale awo mwa mabanja awo, potsata mndandanda wa m'bado wawo, ndi awa:

Yeiyeli, mtsogoleri, Zekariya, 8 ndiponso Bela mwana wa Azazi,
mwana wa Sema, mwana wa Yoweli. Iwo ankakhala ku Aroeri
mpaka ku Nebo ndi Baala-Meoni. 9 Iwo anakhala cha kummawa
mpaka kukafika polowera m'chipululu cha mbali ina ya Mtsinje wa Yufurate, chifukwa ziweto zawo zinaswana kwambiri m'dziko la Giliyadi.

10 Pa nthawi ya Sauli anachita nkhondo ndi Ahagiri ndi kuwagonjetsa. Tsono iwo anakhala m'matenti a Ahagiri ku dera lonse la kummawa kwa Giliyadi.

*Fuko la Gadi*

11 Anthu a fuko la Gadi anakhala moyandikana ndi fuko la Rubeni ku Basani mpaka ku Saleka:

12 Mtsogoleri wawo ku Basani anali Yoweli, wachiwiri anali Safamu, kenaka Yanayi ndi Safati.

13 Abale awo mwa mabanja awo anali awa:

Mikayeli, Mesulamu, Seba, Yorayi, Yakani, Ziya ndi Eberi, onse ali asanu ndi awiri.

14 Amenewa ndiwo anali ana a Abihaili, mwana wa Huri, mwana wa Yarowa, mwana wa Giliyadi, mwana wa Mikayeli, mwana wa Yesisayi, mwana wa Yahido, mwana wa Buzi.

15 Ahi mwana wa Abdieli, mwana wa Guni, anali mtsogoleri wa banja la makolo awo.

16 Fuko la Gadi linakhala ku Giliyadi, ku Basani ndi midzi yozugulira, madera onse a msipu a ku Saroni mpaka kumene amalekezera.

17 Mayina onsewa analembedwa potsata mndandanda wa mibado yawo
pa nthawi ya ulamuliro wa Yotamu mfumu ya Yuda ndi Yeroboamu
mfumu ya Israeli.

18 Mafuko a Rubeni, Gadi ndi theka la Manase, anali ndi anthu 44, 760
okonzeka kulowa usilikali; anthu amatupi amphamvu, amene amatha
kugwiritsa ntchito chishango ndi lupanga, amene amatha kugwiritsa
ntchito uta, amene anaphunzitsidwa kumenya nkhondo. 19 Iwo anachita
nkhondo ndi Ahagiri, Yeturi, Nafisi ndi Nodabu. 20 Iwowo anathandizidwa
polimbana nawo ndipo Mulungu anapereka Ahagiri m'manja mwawo;
popeza iwo anafuwulira kwa Mulungu pa nkhondopo. Iye anayankha
mapemphero awo chifukwa anamudalira. 21 Choncho iwo analanda
ziweto za Ahagiri: ngamira 50,000, nkhosa ndi mbuzi 250,000 ndi abulu
2,000. Ndiponso anagwira akapolo 100,000, 22 enanso ambiri anaphedwa,
chifukwa nkhondoyo inali ya Mulungu. Ndipo iwo anakhala m'dzikomo
mpaka pa nthawi ya ukapolo.

### *Theka la Fuko la Manase*

23 Theka la fuko la Manase linkakhala ku dziko la kummawa kuyambira
ku Basani mpaka ku Baala-Herimoni, kumene ndi ku Seniri (Phiri la
Herimoni) ndipo anthuwo anali ochuluka kwambiri.
24 Atsogoleri a mabanja awo anali awa: Eferi, Isi, Elieli, Azirieli,
Yeremiya, Hodaviya ndi Yahidieli. Iwo anali asilikali olimba mtima, anthu
otchuka, ndiponso atsogoleri a mabanja awo. 25 Koma iwo anali os-
akhulupirika kwa Mulungu wa makolo awo ndipo anadzipereka okha kwa
milungu ya anthu okhala m'dzikomo amene Mulungu anawawononga
pamene iwowo ankafika. 26 Kotero Mulungu wa Israeli anayika mkwiyo
mwa Puli mfumu ya Asuri (ameneyu ndi Tigilati-Pileseri mfumu ya Asuri)
amene anatenga fuko la Rubeni, Gadi ndi theka la fuko la Manase kupita
nawo ku ukapolo. Iye anapita nawo ku Hala, Habori, Hara ndi ku mtsinje
wa Gozani, kumene ali mpaka lero lino.

# 6

### *Fuko la Levi*

1 Ana a Levi anali awa:
Geresoni, Kohati ndi Merari.
2 Ana a Kohati anali awa:
Amramu, Izihari, Hebroni ndi Uzieli.
3 Ana a Amramu anali awa:
Aaroni, Mose ndi Miriamu.
Ana a Aaroni anali awa:
Nadabu, Abihu, Eliezara ndi Itamara
4 Eliezara anabereka Finehasi,
Finehasi anabereka Abisuwa,
5 Abisuwa anabereka Buki,
Buki anabereka Uzi.
6 Uzi anabereka Zerahiya,
Zerahiya anabereka Merayoti,
7 Merayoti anabereka Amariya,
Amariya anabereka Ahitubi.
8 Ahitubi anabereka Zadoki,
Zadoki anabereka Ahimaazi.

9 Ahimaazi anabereka Azariya,
Azariya anabereka Yohanani,
10 Yohanani anabereka Azariya (uyu ndi amene anatumikira monga wansembe m’Nyumba ya Mulungu imene Solomoni anamanga mu Yerusalemu),
11 Azariya anabereka Amariya,
Amariya anabereka Ahitubi,
12 Ahitubi anabereka Zadoki,
Zadoki anabereka Salumu,
13 Salumu anabereka Hilikiya,
Hilikiya anabereka Azariya,
14 Azariya anabereka Seraya,
ndipo Seraya anabereka Yehozadaki.
15 Yehozadaki anagwidwa ukapolo pamene Yehova analola Nebukadinezara kuti agwire ukapolo Yuda ndi Yerusalemu.

16 Ana a Levi anali awa:
Geresomu, Kohati ndi Merari.
17 Mayina a ana a Geresomu ndi awa:
Libini ndi Simei.
18 Ana a Kohati anali awa:
Amramu, Izihari, Hebroni ndi Uzieli.
19 Ana a Merari anali awa:
Mahili ndi Musi.

Mayina a mabanja a fuko la Levi olembedwa potsata makolo awo ndi awa:
20 Ana a Geresomu ndi awa:
Libini, Yehati,
Zima, 21 Yowa,
Ido, Zera
ndi Yeaterai.
22 Zidzukulu za Kohati ndi izi:
Aminadabu, Kora,
Asiri, 23 Elikana,
Ebiyasafu, Asiri,
24 Tahati, Urieli,
Uziya ndi Sauli.
25 Zidzukulu za Elikana ndi izi:
Amasai, Ahimoti,
26 Elikana, Zofai,
Nahati, 27 Eliabu,
Yerohamu, Elikana
ndi Samueli.
28 Ana a Samueli ndi awa:
Mwana wake woyamba anali Yoweli,
wachiwiri anali Abiya.
29 Zidzukulu za Merari ndi izi:
Mahili, Libini,
Simei, Uza,
30 Simea, Hagiya
ndi Asaya.

### *Oyimba m’Nyumba ya Mulungu*

31 Awa ndi anthu amene Davide anawayika kuti aziyang'anira mayim-
bidwe m'Nyumba ya Yehova, Bokosi la Chipangano litabwera kudzakhala
m'menemo. 32 Iwo ankatumikira akuyimba nyimbo pa khomo la malo
opatulika, tenti ya msonkhano, mpaka Solomoni atamanga Nyumba ya
Yehova mu Yerusalemu. Iwo ankagwira ntchito zawo potsata malamulo
amene anawapatsa.

33 Mayina a anthuwo, pamodzi ndi ana awo, anali awa:
Ochokera ku banja la Kohati:
Hemani, katswiri woyimba,
anali mwana wa Yoweli, mwana wa Samueli,
34 mwana wa Elikana, mwana wa Yerohamu,
mwana wa Elieli, mwana wa Towa,
35 mwana wa Zufi, mwana wa Elikana,
mwana wa Mahati, mwana wa Amasai,
36 mwana wa Elikana, mwana wa Yoweli,
mwana wa Azariya, mwana wa Zefaniya,
37 mwana wa Tahati, mwana wa Asiri,
mwana wa Ebiyasafu, mwana wa Kora,
38 mwana wa Izihari, mwana wa Kohati,
mwana wa Levi, mwana wa Israeli;
39 ndi Asafu m'bale wake, amene ankatumikira ku dzanja lake lamanja:
Asafu anali mwana wa Berekiya, mwana wa Simea,
40 mwana wa Mikayeli, mwana wa Baaseya,
mwana wa Malikiya, 41 mwana wa Etini,
mwana wa Zera, mwana wa Adaya,
42 mwana wa Etani, mwana wa Zima,
mwana Simei, 43 mwana wa Yahati,
mwana wa Geresomu, mwana wa Levi;
44 ndipo abale awo ena anali a banja la Merari amene amatumikira ku
dzanja lake lamanzere:
Etani anali mwana wa Kisi, mwana wa Abidi,
mwana wa Maluki, 45 mwana wa Hasabiya,
mwana wa Amaziya, mwana wa Hilikiya,
46 mwana wa Amizi, mwana wa Bani,
mwana wa Semeri, 47 mwana wa Mahili,
mwana wa Musi, mwana wa Merari,
mwana wa Levi.

48 Abale awo Alevi anapatsidwa ntchito zina zonse ku malo opatulika
ku nyumba ya Mulungu. 49 Koma Aaroni ndi zidzukulu zake anali amene
amapereka nsembe pa guwa lansembe zopsereza ndi pa guwa lansembe
zofukiza pamodzi ndi zonse zimene zimachitika ku malo opatulika
kwambiri, kuchita mwambo wopepesera Israeli, potsata zonse zimene
Mose mtumiki wa Mulungu anawalamulira.

50 Ana a Aaroni ndi zidzukulu zake anali awa:
Eliezara, Finehasi,
Abisuwa, 51 Buki,
Uzi, Zerahiya,
52 Merayoti, Amariya,
Ahitubi, 53 Zadoki
ndi Ahimaazi.

54 Malo amene iwo anapatsidwa kuti likhale dziko lawo ndi awa:
(Malowa anapatsidwa kwa zidzukulu za Aaroni zimene zinali za banja
la Kohati, chifukwa malo oyamba kugawidwa anali awo).

55 Iwo anapatsidwa Hebroni m'dziko la Yuda ndi madera odyetsera
ziweto ozungulira malowa. 56 Koma minda ndi midzi yozungulira
mzindawo zinapatsidwa kwa Kalebe mwana wa Yefune.

57 Kotero zidzukulu za Aaroni zinapatsidwa Hebroni (mzinda wop-
ulumukirako), ndi Libina, Yatiri, Esitemowa, 58 Hileni, Debri, 59 Asani,
Yuta ndi Beti-Semesi pamodzi ndi madera odyetsera ziweto ozungulira
malowa. 60 Ndipo ku fuko la Benjamini anapatsidwa Gibiyoni, Geba,
Alemeti ndi Anatoti, pamodzi ndi madera odyetsera ziweto ozungulira
malowa.

Mizinda imene anapatsidwa ku banja la Kohati onse pamodzi inalipo
13.

61 Zidzukulu zotsala za Kohati anazigawira midzi khumi kuchokera ku
mabanja a fuko la theka la Manase.

62 Zidzukulu za Geresomu banja ndi banja zinapatsidwa mizinda 13
kuchokera ku mafuko a Isakara, Aseri ndi Nafutali, ndi gawo lina la fuko
la Manase limene lili ku Basani.

63 Zidzukulu za Merari banja ndi banja zinapatsidwa mizinda khumi ndi
iwiri kuchokera ku mafuko a Rubeni, Gadi ndi Zebuloni.

64 Kotero Aisraeli anapatsa Alevi mizindayi ndi madera a msipu ozun-
gulira malowa. 65 Kuchokera ku mafuko a Yuda, Simeoni ndi Benjamini
anawapatsa mizinda imene inawatchula kale mayina.

66 Mabanja ena a Kohati anapatsidwanso malo kuchokera ku fuko la
Efereimu.

67 Kuchokera ku dziko lamapiri la Efereimu anapatsidwa Sekemu
(mzinda wopulumukirako) ndi Gezeri, 68 Yokineamu, Beti-Horoni,
69 Ayaloni ndi Gati-Rimoni, pamodzi ndi madera odyetsera ziweto
ozungulira.

70 Ndipo kuchokera ku theka la fuko la Manase, Aisraeli anapereka
Aneri ndi Bileamu pamodzi ndi madera odyetsera ziweto kwa mabanja
ena onse a Kohati.

71 Ageresomu analandira malo awa:
Kuchokera ku theka la fuko la Manase,
analandira Golani ku Basani ndiponso Asiteroti, ndi malo awo odyetsera ziweto;
72 Kuchokera ku fuko la Isakara
analandira Kedesi, Daberati, 73 Ramoti ndi Anemu, pamodzi ndi malo ake odyetsera ziweto;
74 kuchokera ku fuko la Aseri
analandira Masala, Abidoni, 75 Hukoki ndi Rehobu, pamodzi ndi malo ake odyetsera ziweto;
76 ndipo kuchokera ku fuko la Nafutali
analandira Kedesi ku Galileya, Hamoni ndi Kiriyataimu, pamodzi ndi malo ake odyetsera ziweto.

77 Amerari (Alevi ena onse) analandira madera awa:
kuchokera ku fuko la Zebuloni,
iwo analandira Yokineamu, Karita, Rimono ndi Tabori, pamodzi ndi malo ake odyetsera ziweto;

78 Kuchokera ku fuko la Rubeni kutsidya kwa Yorodani, kummawa kwa Yeriko,
analandira Bezeri ku chipululu, Yaza, 79 Kedemoti ndi Mefaati,
pamodzi ndi malo ake odyetsera ziweto;
80 ndipo kuchokera ku fuko la Gadi
analandira Ramoti ku Giliyadi, Mahanaimu, 81 Hesiboni ndi Yazeri,
pamodzi ndi malo ake odyetsera ziweto.

# 7

*Fuko la Isakara*

1 Ana a Isakara anali awa:
Tola, Puwa, Yasubu ndi Simironi ndipo onse analipo anayi.
2 Ana a Tola ndi awa:
Uzi, Refaya, Yerieli, Yahimai, Ibisamu ndi Samueli. Awa anali atsogoleri a mabanja awo. Pa nthawi ya ulamuliro wa Davide zidzukulu za Tola zomwe zinali anthu odziwa kumenya nkhondo zinalipo 22,600.
3 Mwana wa Uzi anali
Izirahiya.
Ana a Izirahiya anali:
Mikayeli, Obadiya, Yoweli ndi Isiya. Onse asanu anali atsogoleri a
mabanja. 4 Monga mwa chiwerengero cha mabanja awo, panali
anthu 36,000 odziwa kumenya nkhondo, pakuti iwo anali ndi akazi ndi ana ambiri.
5 Abale awo onse a m'banja la Isakara amene anali odziwa kumenya nkhondo analipo 87,000, olembedwa potsata mibado yawo.

*Fuko la Benjamini*

6 Ana atatu a Benjamini anali awa:
Bela, Bekeri ndi Yediaeli.
7 Ana a Bela anali awa:
Eziboni, Uzi, Uzieli, Yerimoti ndi Iri. Iwowa anali atsogoleri a mabanja awo ndipo onse pamodzi analipo asanu. Pa mndandanda wa m'bado wawo panali anthu 22,034 odziwa kumenya nkhondo.
8 Ana a Bekeri anali awa:
Zemira, Yowasi, Eliezara, Eliyoenai, Omiri, Yeremoti, Abiya, Anatoti
ndi Alemeti. Onsewa anali ana a Bekeri. 9 Pa mndandanda wa
m'bado wawo panali atsogoleri a mabanja ndi anthu 20,200 odziwa kumenya nkhondo.
10 Mwana wa Yediaeli anali
Bilihani.
Ana a Bilihani anali awa:
Yeusi, Benjamini, Ehudi, Kenaana, Zetani, Tarisisi ndi Ahisahara.
11 Ana onsewa a Yediaeli anali atsogoleri a mabanja. Analipo anthu
17,200 amene anali okonzeka kupita ku nkhondo.
12 Asupi ndi Ahupi anali zidzukulu za Iri, ndipo Ahusimu anali zidzukulu za Aheri.

*Fuko la Nafutali*

13 Ana a Nafutali anali awa:
Yahazieli, Guni, Yezeri ndi Salumu, zidzukulu za Biliha.

*Fuko la Manase*

14 Ana a Manase anali awa:

Asirieli ndi mwana amene anabereka kwa mzikazi wake wa ku Aramu. Mzikazi yemweyo anaberekanso Makiri abambo ake a
Giliyadi. 15 Makiri anatenga mkazi wa banja la Ahupi ndi Asupi. Mlongo wake anali Maaka.

Mwana wake wina anali Zelofehadi, amene anabereka ana aakazi okhaokha.

16 Maaka mkazi wa Makiri anabereka mwana wamwamuna ndipo anamutcha Perezi. M'bale wake anamutcha Seresi, ndipo ana ake anali Ulamu ndi Rakemu.

17 Mwana wa Ulamu anali
Bedani.

Awa anali ana a Giliyadi mwana wa Makiri, mwana wa Manase.
18 Mlongo wake Hamoleketi anabereka Isihodi, Abiezeri ndi Mahila.

19 Ana a Semida anali:
Ahiyani, Sekemu, Likihi ndi Aniyamu.

*Fuko la Efereimu*

20 Ana a Efereimu anali awa:
Sutela, Beredi,
Tahati, Eliada,
Tahati, 21 Zabadi,
Sutela.

Ezeri ndi Eladi anaphedwa ndi anthu a ku Gati, pamene anabwera kudzalanda zoweta zawo.
22 Efereimu, abambo awo, anawalira masiku ambiri, ndipo abale ake anabwera kudzamutonthoza.
23 Kenaka anagona ndi mkazi wake, ndipo anakhala woyembekezera nabala mwana wamwamuna. Anamutcha dzina lake Beriya, chifukwa tsoka linagwera banja lake.
24 Mwana wake wamkazi anali Seera, amene anamanga mzinda wa Beti-Horoni Wakumunsi, Wakumtunda kudzanso Uzeni-Seera.

25 Mwana wina wa Efereimu anali Refa amene zidzukulu zake zinali
Resefu,
Tela, Tahani,
26 Ladani, Amihudi,
Elisama, 27 Nuni
ndi Yoswa.

28 Malo amene ankakhala anali Beteli ndi midzi yozungulira, cha kummawa kunali Naarani, Gezeri ndi midzi yake ya kumadzulo ndi Sekemu ndi midzi yake mpaka ku Aya ndi midzi yake.
29 M'mbali mwa malire a Manase munali Beti-Seani, Taanaki, Megido ndi Dori, pamodzi ndi midzi yake. Zidzukulu za Yosefe mwana wa Israeli zimakhala m'mizinda imeneyi.

*Fuko la Aseri*

30 Ana a Aseri anali awa:
Imuna, Isiva, Isivi ndi Beriya. Mlongo wawo anali Sera.

31 Ana a Beriya anali awa:
Heberi ndi Malikieli amene anabereka Birizaiti.

32 Heberi anabereka Yafuleti, Someri, Hotamu ndi Suwa, mlongo wawo.

33 Ana a Yafuleti anali awa:
Pasaki, Bimuhali ndi Asivati.
Awa anali ana a Yafuleti.

34 Ana a Someri anali awa:
Ahi, Rohiga, Yehuba ndi Aramu.

[35] Ana a m'bale wake Helemu anali awa:
Zofa, Imuna, Selesi ndi Amali.
[36] Ana a Zofa anali awa:
Suwa, Harineferi, Suwali, Beri, Imula, [37] Bezeri, Hodi, Sama, Silisa,
Itirani ndi Bera.
[38] Ana a Yeteri anali awa:
Yefune, Pisipa ndi Ara.
[39] Ana a Ula anali awa:
Ara, Hanieli ndi Riziya.

[40] Onsewa anali zidzukulu za Aseri, atsogoleri a mabanja, anthu omveka, ankhondo olimba mtima, ndi akuluakulu pakati pa atsogoleri anzawo. Chiwerengero cha anthu odziwa kumenya nkhondo chomwe chinalembedwa chinali 26,000.

# 8

*Adzukulu a Benjamini ndi Sauli*

[1] Benjamini anabereka Bela mwana wake woyamba,
wachiwiri Asibeli, wachitatu Ahara,
[2] wachinayi Noha ndipo wachisanu Rafa.
[3] Ana a Bela anali awa:
Adari, Gera, Abihudi, [4] Abisuwa, Naamani, Ahowa, [5] Gera, Sefufani ndi
Hiramu.
[6] Zidzukulu za Ehudi, zimene zinali atsogoleri a mabanja a amene amakhala ku Geba ndipo zinasamutsidwa kupita ku Manahati zinali izi:
[7] Naamani, Ahiya ndi Gera, amene anawasamutsa ndipo anabereka Uza ndi Ahihudi.
[8] Saharaimu anabereka ana ku Mowabu atalekana ndi akazi ake,
Husimu ndi Baara. [9] Mwa mkazi wake Hodesi anabereka Yobabu,
Zibiya, Mesa, Malikamu, [10] Yeusi, Sakiya ndi Mirima. Awa ndiye ana
ake, atsogoleri a mabanja awo. [11] Mwa mkazi wake Husimu anabereka
Abitubi ndi Elipaala.
[12] Ana a Elipaala anali awa:
Eberi, Misamu, Semedi (amene anamanga mizinda ya Ono ndi Lodi
ndi midzi yake yozungulira) [13] ndiponso Beriya ndi Sema, amene
anali atsogoleri a mabanja a amene ankakhala ku Ayaloni ndipo
anathamangitsa nzika za ku Gati.
[14] Ahiyo, Sasaki, Yeremoti, [15] Zebadiya, Aradi, Ederi, [16] Mikayeli, Isipa
ndi Yoha anali ana a Beriya.
[17] Zebadiya, Mesulamu, Hiziki, Heberi, [18] Isimerai, Iziliya ndi Yobabu
anali ana a Elipaala.
[19] Yakimu, Zikiri, Zabidi, [20] Elienai, Ziletai, Elieli, [21] Adaya, Beraya ndi
Simirati anali ana a Simei.
[22] Isipani, Eberi, Elieli, [23] Abidoni, Zikiri, Hanani, [24] Hananiya, Elamu,
Anitotiya, [25] Ifideya ndi Penueli anali ana a Sasaki.
[26] Samuserai, Sehariya, Ataliya, [27] Yaaresiya, Eliya ndi Zikiri anali ana a
Yerohamu.
[28] Onsewa anali atsogoleri a mabanja, anthu otchuka potsata mibado yawo, ndipo ankakhala mu Yerusalemu.

[29] Yeiyeli amene amabereka Gibiyoni ankakhala ku Gibiyoni.

Dzina la mkazi wake linali Maaka, 30 ndipo mwana wake woyamba
anali Abidoni, motsatana ndi Zuri, Kisi, Baala, Neri, Nadabu,
31 Gedori, Ahiyo, Zekeri 32 ndi Mikiloti, amene anabereka Simea.
Iwowa ankakhalanso ku Yerusalemu ndi abale awo.
33 Neri anabereka Kisi. Kisi anabereka Sauli, ndipo Sauli anabereka
Yonatani, Maliki-Suwa, Abinadabu ndi Esibaala.
34 Mwana wa Yonatani anali
Meri-Baala, amene anabereka Mika.
35 Ana a Mika anali awa:
Pitoni, Meleki, Tareya ndi Ahazi.
36 Ahazi anabereka Yehoyada, Yehoyada anabereka Alemeti, Azimaveti
ndi Zimuri, ndipo Zimuri anabereka Moza. 37 Moza anabereka
Bineya. Ana ake anali Rafa, Eleasa ndi Azeli.
38 Azeli anali ndi ana asanu ndi mmodzi, ndipo mayina awo anali awa:
Azirikamu, Bokeru, Ismaeli, Seariya, Obadiya ndi Hanani. Onsewa
anali ana a Azeli.
39 Ana a Eseki m'bale wake anali awa:
Mwana wake woyamba Ulamu, wachiwiri Yeusi ndipo wachitatu
Elifeleti. 40 Ana a Ulamu anali asilikali olimba mtima amene
amadziwa kugwiritsa ntchito uta. Iwo anali ndi ana ndi adzukulu
ambiri ndipo onse analipo 150.
Onsewa anali adzukulu a Benjamini.

# 9

1 Aisraeli onse analembedwa potsata mibado yawo m'buku la mafumu a Aisraeli.

### *Anthu a ku Yerusalemu*

Anthu a ku Yuda anatengedwa kunka ku ukapolo ku Babuloni chifukwa
cha kusakhulupirika kwawo. 2 Tsono anthu oyamba kukhala m'madera
awo anali Aisraeli wamba, ansembe, Alevi ndi otumikira ku Nyumba ya
Yehova.

3 Anthu a ku Yuda, Benjamini ndi Efereimu ndiponso Manase amene anakhala mu Yerusalemu anali awa:
4 Utai mwana wa Amihudi, mwana wa Omuri, mwana wa Imuri, mwana
wa Bani, chidzukulu cha Perezi mwana wa Yuda.
5 A banja la Siloni:
Asaya mwana wake woyamba pamodzi ndi ana ake.
6 A banja la Zera:
Yeueli.
Anthu ochokera ku Yuda analipo 690.
7 A fuko la Benjamini:
Salu mwana wa Mesulamu, mwana wa Hodaviya, mwana wa
Hasenuya;
8 Ibineya mwana wa Yerohamu; Ela mwana wa Uzi, mwana wa Mikiri;
ndi Mesulamu mwana wa Sefatiya, mwana wa Reueli mwana wa
Ibiniya.
9 Anthu ochokera ku Benjamini monga analembedwera mwa mibado
yawo, analipo 956. Anthu onsewa anali atsogoleri a mabanja awo.
10 Ansembe:
Yedaya, Yehoyaribu; Yakini;

11 Azariya mwana wa Hilikiya, mwana wa Mesulamu, mwana
wa Zadoki mwana wa Merayoti, mwana wa Ahitubi, wamkulu
woyang'anira Nyumba ya Mulungu;

12 Adaya mwana wa Yerohamu, mwana wa Pasi-Huri, mwana wa
Malikiya; ndi Maasai mwana wa Adieli, mwana wa Yahizera,
mwana wa Mesulamu, mwana wa Mesilemoti, mwana wa Imeri.

13 Ansembe amene anali atsogoleri a mabanja awo analipo 1,760.
Anali anthu amphamvu ndi odziwa kutumikira m'nyumba ya
Mulungu.

14 Alevi:

Semaya mwana wa Hasubu, mwana wa Azirikamu, mwana wa
Hasabiya, wa m'banja la Merari; 15 Bakibakara, Heresi, Galali ndi
Mataniya mwana wa Mika, mwana wa Zikiri, mwana wa Asafu;
16 Obadiya mwana wa Semaya mwana wa Galali, mwana wa
Yedutuni ndi Berekiya mwana wa Asa, mwana wa Elikana, amene
ankakhala ku midzi ya Anetofati.

17 Alonda a pa makomo:

Salumu, Akubu, Talimoni, Ahimani ndi abale awo. Mtsogoleri wawo
anali Salumu. 18 Amenewa amakhala pa chipata cha mfumu
kummawa mpaka lero lino. Alonda a gulu la Alevi anali awa:
19 Salumu mwana wa Kore, mwana wa Ebiyasafu, mwana wa
Kora, pamodzi ndi abale ake a ku banja la makolo ake, Akora aja
ankanyang'anira khomo la Tenti monga ankachitira abambo awo
polondera khomo la malo okhalapo Yehova. 20 Masiku oyamba
Finehasi mwana wa Eliezara anali woyang'anira alonda apakhomo
ndipo Yehova anali naye. 21 Zekariya mwana wa Meselemiya anali
mlonda woyang'anira pa chipata cha tenti ya msonkhano.

22 Onse amene anasankhidwa kukhala alonda pa khonde analipo 212.
Iwo analembedwa mwa mibado yawo ku midzi yawo. Davide ndi
mneneri Samueli ndiwo anawayika m'malo awo antchito chifukwa cha
kukhulupirika kwawo. 23 Iwo ndi zidzukulu zawo anali oyang'anira
zipata za nyumba ya Yehova imene imatchedwa Tenti. 24 Alonda
apakhomowa anali mbali zonse zinayi: kummawa, kumadzulo, kumpoto
ndi kummwera. 25 Abale awo a ku midzi yawo amabwera nthawi ndi
nthawi kudzagwira ntchito yawo kwa masiku asanu ndi awiri. 26 Koma
atsogoleri akuluakulu anayi a alonda, amene anali Alevi, anapatsidwa
udindo woyang'anira zipinda ndi chuma cha nyumba ya Mulungu.
27 Iwo amakhala usiku wonse atayima mozungulira Nyumba ya Mulungu,
chifukwa anayenera kuyilondera. Ndipo anali ndi kiyi wotsekulira
mmawa uliwonse.

28 Ena amayang'anira zipangizo zimene amagwiritsa ntchito pa ntchito
m'Nyumba ya Mulungu. Iwo amaziwerenga zikamalowetsedwa ndi
potulutsidwa. 29 Ena anapatsidwa udindo wosamalira zipangizo ndi
zinthu zina zonse za ku malo opatulika, pamodzi ndi ufa, vinyo, mafuta,
lubani ndi zonunkhira. 30 Koma ansembe ena amasakaniza zonunkhirazo.
31 Mlevi wotchedwa Matitiya mwana woyamba wa Salumu wa m'banja la
Kora, anapatsidwa udindo woyang'anira zophikidwa m'ziwaya. 32 Abale
ake ena a m'banja la Akohati amaphika buledi wa pa Sabata lililonse
amene amayikidwa pa tebulo.

33 Atsogoleri a mabanja a Alevi, amene anali ndi luso loyimba, amakhala
m'zipinda za Nyumba ya Mulungu ndipo samagwira ntchito zina chifukwa

ankatumikira usana ndi usiku.
34 Onsewa anali atsogoleri a mabanja a Alevi, akuluakulu monga
analembedwera pa mibado yawo, ndipo ankakhala mu Yerusalemu.

### *Mibado ya Sauli*

35 Yeiyeli abambo a Gibiyoni ankakhala ku Gibiyoni.
Dzina la akazi awo linali Maaka, 36 ndipo mwana wawo woyamba
kubadwa anali Abidoni, motsatana ndi Zuri, Kisi, Baala, Neri, Nad-
abu, 37 Gedori, Ahiyo, Zekariya ndi Mikiloti. 38 Mikiloti anabereka
Simeamu. Iwonso ankakhala ndi abale awo ku Yerusalemu.
39 Neri anabereka Kisi, Kisi anabereka Sauli, ndipo Sauli anabereka
Yonatani, Maliki-Suwa, Abinadabu ndi Esibaala.
40 Mwana wa Yonatani anali
Meri-Baala, amene anabereka Mika.
41 Ana a Mika anali:
Pitoni, Meleki, Tahireya ndi Ahazi.
42 Ahazi anabereka Yara, Yara anabereka Alemeti, Azimaveti ndi
Zimuri, ndipo Zimiri anabereka Moza. 43 Moza anabereka Bineya.
Ana ake anali Refaya, Eleasa ndi Azeli.
44 Azeli anali ndi ana asanu ndi mmodzi ndipo mayina awo anali awa:
Azirikamu, Bokeru, Ismaeli, Seariya, Obadiya ndi Hanani. Awa anali
ana a Azeli.

# 10

### *Sauli Adzipha Yekha*

1 Tsono Afilisti anachitanso nkhondo ndi Aisraeli ndipo Aisraeli
anathawa Afilistiwo, kotero kuti ambiri anaphedwa pa phiri la Gilibowa.
2 Afilisti anapanikiza kwambiri Sauli ndi ana ake, ndipo anapha Yonatani,
Abinadabu ndi Maliki-Suwa. 3 Nkhondo inakula kwambiri mozungulira
Sauli ndipo pamene anthu amauta anamupeza, anamuvulaza.
4 Tsono Sauli anawuza mnyamata wake wonyamula zida zake kuti,
"Solola lupanga lako undiphe, kuopa kuti anthu osachita mdulidwewa
angabwere ndi kudzandizunza ine."
Koma mnyamata wonyamula zida uja anachita mantha kwambiri ndipo
sanathe kutero. Choncho Sauli anatenga lupanga lake lomwe nagwerapo.
5 Mnyamata wonyamula zida zake uja ataona kuti Sauli wafa, nayenso
anadzigwetsera pa lupanga lake nafa. 6 Motero Sauli ndi ana ake atatu
anafa, pamodzi ndi banja lake lonse anafera limodzi.
7 Pamene Aisraeli onse amene anali m'chigwa anaona kuti gulu
lankhondo lathawa komanso kuti Sauli ndi ana ake aphedwa, nawonso
anathawa kusiya mizinda yawo. Ndipo Afilisti anabwera kudzakhalamo.
8 Mmawa mwake, Afilisti atabwera kudzatenga zinthu za anthu
ophedwa, anapeza Sauli ndi ana ake atafa pa phiri la Gilibowa. 9 Iwo
anamuvula zovala zake, natenga mutu wake ndi zida zake zankhondo.
Ndipo anatumiza amithenga m'dziko lonse la Afilisti kukafalitsa nkhani
yabwinoyi kwa mafano awo ndi kwa anthu awo. 10 Iwo anayika zida zake
zankhondo m'nyumba zopembedzera milungu yawo ndipo anapachika
mutu wake m'nyumba ya Dagoni.
11 Pamene anthu onse okhala ku Yabesi Giliyadi anamva zimene Afilisti
anachitira Sauli, 12 anthu awo onse olimba mtima anapita kukatenga
mitembo ya Sauli ndi ana ake ndipo anabwera nayo ku Yabesi. Anakwirira

mafupa awo pansi pa mtengo wabwemba ku Yabesi, ndipo anasala kudya masiku asanu ndi awiri.
13 Sauli anafa chifukwa anali wosakhulupirika pamaso pa Yehova. Iye sanasunge mawu a Yehova, pakuti anakafunsira nzeru kwa woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa,
14 sanafunsire nzeruzo kwa Yehova. Choncho Yehova anamupha ndi kupereka ufumu kwa Davide mwana wa Yese.

# 11

### *Davide Adzozedwa Kukhala Mfumu ya Israeli*

1 Aisraeli onse anasonkhana pamaso pa Davide ku Hebroni ndipo anati, "Ife ndife abale anu.
2 Kale lija, ngakhale pamene Sauli anali mfumu, inu ndinu amene munkatsogolera Aisraeli pa nkhondo zawo. Ndipo Yehova Mulungu wanu anakuwuzani kuti, 'Iwe udzaweta anthu anga Aisraeli, ndipo udzakhala mfumu yawo.' "
3 Akuluakulu onse a Israeli atafika kwa Mfumu Davide ku Hebroni, iye anachita nawo pangano pamaso pa Yehova, ndipo anamudzoza Davide kukhala mfumu ya Israeli, monga momwe Yehova analonjezera kudzera mwa Samueli.

### *Davide Agonjetsa Yerusalemu*

4 Davide ndi Aisraeli onse anapita ku Yerusalemu (ku Yebusi). Ayebusi amene ankakhala kumeneko
5 anamuwuza Davide kuti, "Simulowa muno." Komabe Davide analanda linga la Ziyoni, limene ndi mzinda wa Davide.
6 Davide anali atanena kuti "Aliyense amene adzatsogolere kukathira nkhondo Ayebusi adzakhala mkulu wa asilikali." Yowabu mwana wa Zeruya ndiye anayamba kupita, motero anakhala mkulu wa asilikali.
7 Tsono Davide anakhazikika mu lingamo, ndipo mzindawu anawutcha Mzinda wa Davide.
8 Iye anamanga malo onse ozungulira, kuyambira ku matsitso ozungulira khoma. Ndipo Yowabu anakonzanso mbali ina ya mzindawu.
9 Ndipo mphamvu za Davide zinkakulirakulira chifukwa anali ndi Yehova Wamphamvuzonse.

### *Asilikali Otchuka a Davide*

10 Awa ndiye anali atsogoleri amphamvu a Davide. Iwo pamodzi ndi Aisraeli onse, anathandiza kulimbikitsa ufumu wake kuti ukwanire madera onse, monga momwe Yehova analonjezera.
11 Nawa mayina a ankhondo amphamvu a Davide:
Yasobeamu Mhakimoni anali mkulu wa atsogoleri. Iye anapha ndi mkondo ankhondo 300 nthawi imodzi.
12 Wotsatana naye anali Eliezara mwana wa Dodo Mwahohi, mmodzi mwa ankhondo atatu amphamvu.
13 Iye anali ndi Davide ku Pasi-Damimu pamene Afilisti anasonkhana kudzachita nkhondo. Ankhondo anathawa Afilistiwo pamalo pamene panali munda wodzaza ndi barele.
14 Koma awiriwo anayima pakati pa mundawo. Iwo anawuteteza, nakantha Afilistiwo ndipo Yehova anawapambanitsa koposa.
15 Atatu mwa atsogoleri makumi atatu aja anabwera kwa Davide ku thanthwe ku phanga la Adulamu pamene gulu la Afilisti linali litamanga misasa m'chigwa cha Refaimu.
16 Nthawi imeneyo Davide anali mu linga, ndipo boma la Afilisti linali ku Betelehemu.
17 Davide analakalaka madzi ndipo anati, "Haa, pakanapezeka munthu wokanditungira madzi a m'chitsime chomwe chili pafupi ndi chipata cha ku Betelehemu!"

18 Choncho anthu atatuwa anadutsa mizere ya Afilisti, natunga madzi
amene anali m'chitsime chomwe chinali pafupi ndi chipata cha ku
Betelehemu nabwera nawo kwa Davide. Koma iye anakana kumwa.
M'malo mwake anathira pansi pamaso pa Yehova. 19 Iye anati, "Inu
Mulungu, musalole kuti ine ndichite chinthu ichi! Kodi ndimwe magazi
a anthu amene anayika miyoyo yawo pachiswe?" Chifukwa iwo anayika
miyoyo yawo pachiswe kuti abweretse madziwo, Davide sanamwe.
Zimenezi ndi zimene anachita anthu amphamvu atatuwo.

20 Abisai m'bale wa Yowabu ndiye anali mtsogoleri wa anthu atatuwa.
Iye anapha ndi mkondo ankhondo 300. Choncho iyeyo anali wotchuka
pakati pa anthu atatu aja. 21 Iye analandira ulemu woposa atatuwo. Kotero
anakhala mtsogoleri wawo ngakhale kuti iyeyo sanali m'gulu la anthu
atatu aja.

22 Benaya mwana wa Yehoyada wa ku Kabizeeli anali munthu wolimba
mtima amene anachita zinthu zamphamvu. Iye anakantha ankhondo
awiri otchuka a ku Mowabu. Tsiku lina kukuzizira kwambiri, iye
analowa m'dzenje ndi kuphamo mkango. 23 Ndipo iye anakanthanso
Mwigupto amene anali wotalika mamita awiri ndi theka. Ngakhale kuti
Mwiguptoyo anali ndi mkondo wofanana ndi ndodo yowombera nsalu
m'dzanja mwake, Benaya anapita kukamenyana naye ali ndi chibonga
chokha m'manja. Iye analanda mkondo m'dzanja la Mwiguptoyo ndi
kumupha ndi mkondo wake womwe. 24 Izi ndi zamphamvu zimene
Benaya mwana wa Yehoyada anachita. Iyeyo analinso wotchuka ngati
anthu atatu amphamvu aja. 25 Iye ankalemekezedwa kuposa wina aliyense
mwa anthu makumi atatu, koma sanali m'gulu la anthu atatu aja. Ndipo
Davide anamuyika kukhala woyang'anira asilikali omuteteza.

26 Ankhondo amphamvuwa anali:
Asaheli m'bale wa Yowabu,
Elihanani mwana wa Dodo wa ku Betelehemu,
27 Samoti Mharori,
Helezi Mpeloni.
28 Ira mwana wa Ikesi wa ku Tekowa,
Abiezeri wa ku Anatoti,
29 Sibekai Mhusati,
Ilai Mwahohi,
30 Maharai Mnetofa,
Heledi mwana wa Baana Mnetofa,
31 Itai mwana wa Ribai wa ku Gibeya ku Benjamini,
Benaya Mpiratoni,
32 Hurai wa ku zigwa za Gaasi,
Abieli Mwaribati,
33 Azimaveti Mbaharumi,
Eliyahiba Msaaliboni,
34 ana a Hasemu Mgizoni,
Yonatani mwana wa Sage Mharari,
35 Ahiamu mwana wa Sakari Mharari,
Elifali mwana wa Uri,
36 Heferi Mmekerati,
Ahiya Mpeloni,
37 Heziro wa ku Karimeli
Naara mwana wa Ezibai,

38 Yoweli m'bale wa Natani,
Mibihari mwana wa Hagiri,
39 Zeleki Mwamoni,
Naharai wa ku Beeroti, mnyamata wonyamula zida za Yowabu mwana wa Zeruya.
40 Ira Mwitiri,
Garebu Mwitiri,
41 Uriya Mhiti,
Zabadi mwana wa Ahilai,
42 Adina mwana wa Siza Mrubeni, amene anali mtsogoleri wa Arubeni ndi anthu makumi atatu pamodzi naye,
43 Hanani mwana wa Maaka,
Yehosafati Mmitini,
44 Uziya Mwasiterati,
Sama ndi Yeiyeli ana a Hotamu Mwaroeri,
45 Yediaeli mwana wa Simiri,
ndi Yoha Mtizi m'bale wake,
46 Elieli Mhavati,
Yeribai ndi Yosaviya ana a Elinaamu,
Itima Mmowabu,
47 Elieli, Obedi ndi Yaasieli Mmeobai.

# 12

### *Ankhondo Amene Anali ndi Davide, Sauli Asanafe*

1 Nawa anthu amene anabwera kwa Davide ali ku Zikilagi pamene
iye anathamangitsidwa ndi Sauli mwana wa Kisi (iwowo anali m'gulu
la asilikali amene ankamuthandiza pa nkhondo. 2 Iwo anali ndi mauta
ndipo amadziwa kuponya mivi komanso miyala, ndipo amatha kuponyera
dzanja lamanja kapena lamanzere. Iwo anali abale ake a Sauli ochokera
ku fuko la Benjamini.

3 Mtsogoleri wawo anali Ahiyezeri ndi Yowasi ana a Semaya wa
ku Gibeya; Yezieli ndi Peleti ana a Azimaveti; Beraka, Yehu wa ku
Anatoti, 4 ndi Isimaiya wa ku Gibiyoni, munthu wamphamvu m'gulu la
anthu makumi atatu aja, yemwenso anali mtsogoleri wawo; Yeremiya,
Yahazieli, Yohanani, Yozabadi wa ku Gederi, 5 Eluzai, Yerimoti, Bealiya,
Semariya ndi Sefatiya Mharufi; 6 Elikana, Isiya, Azareli, Yowezeri ndi
Yasobeamu a ku banja la Kora; 7 ndi Yowela ndi Zebadiya ana a
Yerohamu wa ku Gedori.

8 Asilikali ena a fuko la Gadi anathawira kwa Davide ku linga lake ku
chipululu. Iwo anali asilikali olimba mtima, okonzekera nkhondo ndipo
amadziwa kugwiritsa ntchito chishango ndi mkondo. Iwowo anali woopsa
ngati mikango ndipo anali aliwiro ngati ngoma zam'mapiri.
9 Mtsogoleri wawo anali Ezeri,
wotsatana naye anali Obadiya, wachitatu anali Eliabu,
10 wachinayi anali Misimana, Yeremiya anali wachisanu,
11 wachisanu ndi chimodzi anali Atai, Elieli anali wachisanu ndi chiwiri,
12 wachisanu ndi chitatu anali Yohanani, Elizabadi anali wachisanu ndi chinayi,
13 wakhumi anali Yeremiya ndipo Makibanai anali wa 11.

14 Anthu a fuko la Gadi amenewa anali atsogoleri; ang'onoang'ono amalamulira anthu 100 pamene akuluakulu amalamulira anthu 1,000.
15 Awa ndi amene anawoloka Yorodani mwezi woyamba pamene mtsinje unali utasefukira mbali zonse, ndipo anathamangitsa aliyense amene amakhala m'chigwa, mbali ya kumadzulo ndi kummawa.

16 Anthu ena a fuko la Benjamini ndi ena ochokera ku Yuda anabwer-
anso kwa Davide pamene anali ku linga lake. 17 Davide anapita kukaku-
mana nawo ndipo anati, "Ngati mwabwera kwa ine mwamtendere, kuti mundithandize, ndakonzeka kugwirizana nanu. Koma ngati mwabwera kudzandipereka kwa adani anga, ngakhale kuti sindinalakwe, Mulungu wa makolo anthu aone izi ndipo akuweruzeni."

18 Kenaka Mzimu anabwera pa Amasai, mtsogoleri wa anthu makumi atatu aja ndipo anati:

"Inu Davide, ife ndife anu!
Tili nanu limodzi, inu mwana wa Yese!
Kupambana, Kupambana kwa inu,
ndiponso kupambana kukhale kwa iwo amene akukuthandizani
pakuti Mulungu wanu adzakuthandizani."

Kotero Davide anawalandira ndipo anawayika kukhala atsogoleri a magulu ake a ankhondo.

19 Anthu ena a fuko la Manase anathawira kwa Davide pamene anapita
ndi Afilisti kukamenyana ndi Sauli. (Iye ndi anthu ake sanathandize Afilisti chifukwa, atsogoleri awo atakambirana, anamubweza Davide. Iwo anati, "Ife tidzawonongedwa ngati uyu adzabwerera kwa mbuye wake
Sauli)." 20 Davide atapita ku Zikilagi, anthu a fuko la Manase amene anathawira kwa iye anali awa: Adina, Yozabadi, Yediaeli, Mikayeli, Yozabadi, Elihu ndi Ziletai; atsogoleri a magulu a anthu 1,000 a ku Manase.
21 Iwowa anathandiza Davide kulimbana ndi magulu achifwamba, pakuti onsewa anali asilikali olimba mtima ndipo anali atsogoleri m'gulu lake
la ankhondo. 22 Tsiku ndi tsiku anthu amabwera kudzathandiza Davide, mpaka anakhala ndi gulu lalikulu la ankhondo, ngati gulu la ankhondo a Mulungu.

### *Enanso Abwera kwa Davide ku Hebroni*

23 Nachi chiwerengero cha magulu a anthu ankhondo amene anabwera kwa Davide ku Hebroni kudzapereka ufumu wa Sauli kwa iye, monga momwe ananenera Yehova:

24 Anthu a fuko la Yuda onyamula chishango ndi mkondo analipo 6,800;
25 Anthu a fuko la Simeoni, asilikali okonzekera nkhondo analipo 7,100;
26 Anthu a fuko la Levi analipo 4,600, 27 mtsogoleri Yehoyada wa banja
la Aaroni anabweranso ndi anthu 3,700, 28 ndi Zadoki, mnyamata wankhondo wolimba mtima, anabwera ndi akuluakulu 22 ochokera m'banja lake;
29 Anthu a fuko la Benjamini, abale ake a Sauli analipo 3,000 ndipo ambiri anali ndi Sauli ku nyumba yake pa nthawiyi;
30 Anthu a fuko la Efereimu, asilikali olimba mtima, otchuka pa mabanja awo analipo 20,800;
31 Anthu a fuko latheka la Manase amene anawayitana kuti adzakhazikitse nawo ufumu wa Davide analipo 18,000;
32 Anthu a fuko la Isakara amene ankazindikira nthawi ndipo amadziwa zimene Israeli ankayenera kuchita, analipo atsogoleri 200 pamodzi ndi abale awo onse amene amawatsogolera.

33 Anthu a fuko la Zebuloni, analipo 5,000. Iwowa anali asilikali odziwa
bwino nkhondo, okhala ndi zida za mtundu uliwonse, okonzekera
kudzathandiza Davide ndi mtima umodzi.

34 Anthu a fuko la Nafutali, analipo atsogoleri 1,000 pamodzi ndi anthu
37,000 onyamula zishango ndi mikondo;

35 Anthu a fuko la Dani, okonzekera nkhondo analipo 28,600.

36 Anthu a fuko la Aseri, asilikali odziwa bwino nkhondo, okonzekeradi
nkhondo analipo 40,000;

37 Ndipo kuchokera kummawa kwa Yorodani, anthu a fuko la Rubeni,
Gadi ndi theka la fuko la Manase, amene anali ndi zida za mtundu
uliwonse analipo 120,000.

38 Onsewa anali anthu odziwa kumenya nkhondo amene anadzipereka
ku magulu awo. Iwo anabwera ku Hebroni ali otsimikiza kudzamuyika
Davide kukhala mfumu ya Aisraeli. Aisraeli ena onse anali ndi mtima
umodzinso womuyika Davide kukhala mfumu. 39 Anthuwa anakhala ndi
Davide masiku atatu akudya ndi kumwa pakuti mabanja awo anawapatsa
zakudya. 40 Komanso anthu oyandikana nawo ochokera ku Isakara,
Zebuloni ndi Nafutali anabweretsa zakudya pa abulu, ngamira, nyulu ndi
ng'ombe. Panali ufa wambiri, makeke ankhuyu, ntchintchi za mphesa,
vinyo, mafuta, ng'ombe, nkhosa ndi mbuzi, popeza munali chimwemwe
mu Israeli.

# 13

### *Abweretsanso Bokosi la Chipangano*

1 Davide anakambirana ndi akuluakulu ake, atsogoleri a anthu 1,000
ndi atsogoleri a anthu 100. 2 Ndipo anati kwa gulu lonse la Israeli, "Ngati
kukukomerani komanso ngati chili chifuniro cha Yehova Mulungu wathu,
tiyeni titumize uthenga kulikonse kumene kuli abale athu ena onse ku
dziko lonse la Israeli ndiponso kwa ansembe ndi Alevi amene ali nawo
m'midzi yawo ndi madera odyetsera ziweto, kuti abwere adzakhale nafe.
3 Tiyeni tibweretsenso Bokosi la Mulungu wathu kuno kwathu, pakuti
nthawi ya Sauli sitinafunse za bokosili." 4 Gulu lonse linavomereza izi,
pakuti anthu onse anaona kuti kunali kofunika kutero.

5 Kotero Davide anasonkhanitsa Aisraeli onse, kuchokera ku mtsinje
wa Sihori ku Igupto mpaka ku Lebo Hamati, kuti abweretse Bokosi la
Mulungu kuchokera ku Kiriati-Yearimu. 6 Davide pamodzi ndi Aisraeli
onse anapita ku Baalahi (Kiriati-Yearimu) ku Yuda kukatenga Bokosi la
Yehova Mulungu, amene amakhala pakati pa akerubi. Limeneli ndiye
Bokosi la Chipangano lomwe limadziwika ndi Dzina lake.

7 Iwo anachotsa Bokosi la Mulungu ku nyumba ya Abinadabu pa
ngolo yatsopano. Uza ndi Ahiyo ndiwo ankayendetsa ngoloyo. 8 Davide
pamodzi ndi Aisraeli onse ankakondwerera ndi mphamvu zawo zonse
pamaso pa Mulungu, poyimba nyimbo pogwiritsa ntchito azeze, apangwe,
matambolini, maseche ndi malipenga.

9 Atafika pa malo opunthira tirigu ku Kidoni, Uza anatambalitsa dzanja
lake kuti agwire bokosilo, chifukwa ng'ombe zinkafuna kugwa. 10 Yehova
anapsera mtima Uza ndipo anamukantha chifukwa chogwira bokosilo.
Choncho iyeyo anafera pomwepo pamaso pa Mulungu.

11 Ndipo Davide anakhumudwa chifukwa Yehova anakantha Uza ndipo
mpaka lero malowo amatchedwa Perezi Uza.

12 Tsiku limenelo Davide anachita mantha ndi Mulungu ndipo ana-
funsa kuti, “Kodi Bokosi la Mulungu lingafike bwanji kwathu?” 13 Iye
sanapitenso nalo Bokosi la Mulungu ku Mzinda wa Davide. M’malo
mwake anapita nalo ku nyumba ya Obedi-Edomu Mgiti. 14 Ndipo
Bokosi la Mulungu linakhala m’banja la Obedi-Edomu m’nyumba mwake
kwa miyezi itatu ndipo Yehova anadalitsa nyumba yake ndi chilichonse
chimene anali nacho.

# 14

### *Nyumba ya Davide ndi Banja Lake*

1 Hiramu mfumu ya ku Turo inatumiza amithenga kwa Davide pamodzi
ndi mitengo ya mkungudza ndiponso amisiri a miyala ndi amisiri a
matabwa kuti adzamumangire nyumba yaufumu. 2 Choncho Davide
anazindikira kuti Yehova wamukhazikitsa kukhala mfumu ya Israeli ndipo
wakuza kwambiri ufumu wake chifukwa cha anthu ake, Aisraeli.
3 Davide anakwatira akazi ena ambiri ku Yerusalemu ndipo anabereka
ana aamuna ndi aakazi ambiri. 4 Mayina a ana amene anaberekera ku
Yerusalemu anali awa: Samua, Sobabu, Natani, Solomoni, 5 Ibihari, Elisua,
Elipeleti, 6 Noga, Nefegi, Yafiya, 7 Elisama, Beeliada ndi Elifeleti.

### *Davide Agonjetsa Afilisti*

8 Afilisti atamva kuti Davide wadzozedwa kukhala mfumu ya dziko lonse
la Israeli, iwo anapita mwamphamvu kukamusakasaka. Koma Davide
atamva zimenezi anapita kukakumana nawo. 9 Ndipo Afilisti anabwera
ndi kulanda zinthu m’Chigwa cha Refaimu. 10 Davide anafunsa Mulungu
kuti, “Kodi ndipite kukathira nkhondo Afilisti? Kodi mukawapereka
m’manja mwanga?”
Yehova anamuyankha kuti, “Pita, Ine ndidzawapereka m’manja
mwako.”
11 Choncho Davide ndi anthu ake anapita ku Baala-Perazimu ndi
kugonjetsa Afilistiwo. Iye anati, “Monga amasefukira madzi, Mulungu
waphwanya adani anga ine ndikuona.” Motero anawatcha malowa Baala
Perazimu. 12 Afilisti anasiya milungu yawo kumeneko ndipo Davide
analamulira kuti itenthedwe ndi moto.
13 Nthawi inanso Afilisti anadzalanda katundu mu Chigwamo.
14 Choncho Davide anafunsa Mulungu ndipo Mulunguyo anayankha kuti,
“Usapite molunjika, koma uzungulire kumbuyo kwawo. Ukawathire
nkhondo patsogolo pa mitengo ya mkandankhuku. 15 Mukakangomva
phokoso pa msonga za mitengo ya mkandankhuku, mukapite kuka-
menyana nawo, chifukwa izi zikasonyeza kuti Mulungu ali patsogolo
panu kukantha ankhondo a Afilisti.” 16 Kotero Davide anachita zimene
Mulungu anamulamulira ndipo anakantha ankhondo a Afilisti njira yonse
kuchokera ku Gibiyoni mpaka ku Gezeri.
17 Choncho mbiri ya Davide inafalikira dziko lonse, ndipo Yehova
anachititsa kuti mayiko ena azimuopa.

# 15

### *Bokosi la Chipangano Alibweretsa ku Yerusalemu*

1 Davide atadzimangira nyumba zina mu Mzinda wa Davide, iye
anakonza malo a Bokosi la Mulungu ndipo analimangira tenti. 2 Pamenepo
Davide anati, “Palibe wina ati anyamule Bokosi la Mulungu koma Alevi

chifukwa Yehova anawasankha kuti azinyamula Bokosi la Yehova ndi kumatumikira pamaso pake nthawi zonse."

3 Davide anasonkhanitsa Aisraeli onse mu Yerusalemu kuti abweretse
Bokosi la Yehova ku malo amene analikonzera. 4 Iye anayitanitsa pamodzi
zidzukulu za Aaroni ndi Alevi:

5 kuchokera ku banja la Kohati,
mtsogoleri Urieli ndi abale ake 120.
6 Kuchokera ku banja la Merari,
mtsogoleri Asaya ndi abale ake 220;
7 kuchokera ku banja la Geresomu,
mtsogoleri Yoweli ndi abale ake 130;
8 kuchokera ku banja la Elizafani,
mtsogoleri Semaya ndi abale ake 200;
9 kuchokera ku banja la Hebroni,
mtsogoleri Elieli ndi abale ake 80;
10 kuchokera ku banja la Uzieli,
mtsogoleri Aminadabu ndi abale ake 112.

11 Kenaka Davide anayitanitsa ansembe Zadoki ndi Abiatara, ndi Alevi
awa, Urieli, Asaya, Yoweli, Semaya, Elieli ndi Aminadabu. 12 Iye
anawawuza kuti, "Inu ndinu atsogoleri a mabanja a Alevi ndipo inu ndi
abale anu Alevi mudziyeretse nokha ndi kubweretsa Bokosi la Yehova Mu-
lungu wa Israeli ku malo amene ine ndalikonzera. 13 Popeza kuti inu Alevi
simunalinyamule poyamba paja, Yehova Mulungu wathu anatikantha.
Sitinafunse momwe tikanachitira monga mmene Iyeyo anafotokozera."
14 Kotero ansembe ndi Alevi anadziyeretsa ndi cholinga chakuti akatenge
Bokosi la Yehova Mulungu wa Israeli. 15 Ndipo Alevi ananyamula Bokosi la
Mulungu pa mapewa awo pa mitengo yake yonyamulira monga momwe
Mose analamulira molingana ndi mawu a Yehova.

16 Davide anawuza atsogoleri a Alevi kuti asankhe abale awo kuti akhale
oyimba nyimbo zachisangalalo, zoyimba ndi zida: azeze, apangwe ndi
ziwaya za malipenga.

17 Kotero Alevi anasankha Hemani mwana wa Yoweli; ndipo mwa abale
ake anasankha Asafu mwana wa Berekiya; ndipo mwa ana a Merari, abale
awo, anasankha Etani mwana wa Kusaya; 18 ndipo pamodzi ndi iwowa
abale awo otsatana nawo: Zekariya, Yaazieli, Semiramoti, Yehieli, Uni,
Eliabu, Benaya, Maaseya, Matitiya, Elifelehu, Mikineya, Obedi-Edomu ndi
Yeiyeli, alonda a pa chipata.

19 Anthu oyimba aja Hemani, Asafu ndi Etani ndiwo ankayimba
ziwaya za malipenga zamkuwa; 20 Zekariya, Azieli, Semiramoti, Yehieli,
Uni, Eliabu, Maaseya ndi Benaya ankayimba azeze a liwu lokwera;
21 ndipo Matitiya, Elifelehu, Mikineya, Obedi-Edomu, Yeiyeli ndi Azaziya
ankayimba apangwe a liwu lotsika. 22 Kenaniya, mtsogoleri wa Alevi anali
woyang'anira mayimbidwe; uwu ndiye unali udindo wake pakuti anali
waluso pa zimenezi.

23 Berekiya ndi Elikana anali olondera pa khomo la bokosilo. 24 Ansembe
awa; Sebaniya, Yehosafati, Netaneli, Amasai, Zekariya, Benaya ndi Eliezara
ndiwo ankayimba malipenga patsogolo pa Bokosi la Mulungu. Obedi-
Edomu ndi Yehiya analinso alonda a pa khomo la bokosilo.

25 Choncho Davide pamodzi ndi akuluakulu a Israeli ndiponso asilikali olamulira magulu a anthu 1,000, anapita kukatenga Bokosi la Chipangano
la Yehova ku nyumba ya Obedi-Edomu akukondwera. 26 Popeza Mulungu
anathandiza Alevi amene ananyamula Bokosi la Chipangano la Yehova, anapereka nsembe ng'ombe zazimuna zisanu ndi ziwiri ndiponso nkhosa
zazimuna zisanu ndi ziwiri. 27 Ndipo Davide anali atavala mkanjo
wa nsalu yofewa yosalala, monga anavalira Alevi onse amene ananyamula bokosi pamodzi anthu oyimba, ndiponso Kenaniya, amene anali
woyang'anira magulu oyimba. Davide anavalanso efodi ya nsalu yofewa
yosalala. 28 Kotero Aisraeli onse anabweretsa Bokosi la Chipangano la
Yehova ndi mfuwu, ndiponso akuyimba zitoliro zanyanga zankhosa zazimuna, malipenga ndi maseche ndiponso akuyimba azeze ndi apangwe.
29 Bokosi la Chipangano la Yehova likulowa mu Mzinda wa Davide, Mikala mwana wamkazi wa Sauli ankaona ali pa zenera. Ndipo ataona
Mfumu Davide ikuvina ndi kukondwera, iye ananyoza Davideyo mu mtima mwake.

# 16

1 Iwo anabwera nalo Bokosi la Mulungu ndipo analiyika pamalo pake m'kati mwa tenti imene Davide anayimika ndipo iwo anapereka nsembe
zopsereza ndi nsembe zachiyanjano pamaso pa Mulungu. 2 Davide atatsiriza kupereka nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano, iye
anadalitsa anthu m'dzina la Yehova. 3 Kenaka anagawira Mwisraeli aliyense, wamwamuna ndi wamkazi, aliyense buledi mmodzi, nthuli yanyama ndiponso keke yamphesa zowuma.
4 Iye anasankha Alevi ena kuti azitumikira pamene panali Bokosi la Yehova, kuti azipemphera, azithokoza ndi kulemekeza Yehova Mulungu
wa Israeli. 5 Mtsogoleri wawo anali Asafu, wachiwiri anali Zekariya, kenaka Yeiyeli, Semiramoti, Yehieli, Matitiya, Eliabu, Benaya, Obedi-Edomu ndi Yeiyeli. Iwo amayimba azeze ndi apangwe, Asafu amayimba
ziwaya za malipenga, 6 ndipo ansembe Benaya ndi Yahazieli amawomba malipenga nthawi zonse pamaso pa Bokosi la Chipangano la Mulungu.

### *Nyimbo Yotamanda ya Davide*

7 Tsiku limeneli Davide anayamba n'kusankha Asafu ndi anzake kuti ndiwo apereke nyimbo iyi ya matamando kwa Yehova:

8 Yamikani Yehova, itanani dzina lake;
lalikani za ntchito zake pakati pa mitundu ya anthu.
9 Imbirani Iye, muyimbireni nyimbo zamatamando;
nenani za ntchito zake zonse zodabwitsa.
10 Nyadirani dzina lake loyera;
ikondwere mitima ya iwo akufunafuna Yehova.
11 Dalirani Yehova ndi mphamvu zake;
funafunani nkhope yake nthawi zonse.
12 Kumbukirani ntchito zodabwitsa wazichita,
zozizwitsa zake, ndi kuweruza kwa m'kamwa mwake,
13 inu zidzukulu za Israeli mtumiki wake,
inu ana a Yakobo, osankhidwa ake.

14 Iye ndiye Yehova Mulungu wathu;
chiweruzo chake chili pa dziko lonse lapansi.
15 Iye amakumbukira pangano lake nthawi zonse,

mawu amene Iye analamula, kwa mibado miyandamiyanda,
16 pangano limene anachita ndi Abrahamu,
lonjezo limene analumbira kwa Isake.
17 Iye analitsimikiza kwa Yakobo monga lamulo,
kwa Israeli monga pangano lamuyaya.
18 "Kwa iwe, ine ndidzapereka dziko la Kanaani
monga cholowa chimene udzachilandira."

19 Ali anthu owerengeka,
ochepa ndithu, komanso alendo m'dzikomo,
20 iwo anayendayenda kuchoka ku mtundu wina kupita ku mtundu wina,
ku ufumu wina kupita ku ufumu wina.
21 Iye sanalole munthu aliyense kuti awapondereze;
chifukwa cha iwo, Iye anadzudzula mafumu:
22 "Musakhudze odzozedwa anga;
musawachitire choyipa aneneri anga."

23 Imbirani Yehova, dziko lonse lapansi;
lalikani za chipulumutso chake tsiku ndi tsiku.
24 Lengezani za ulemerero wake kwa mitundu yonse,
ntchito zake zonse zodabwitsa kwa anthu onse.
25 Pakuti Yehova ndi wamkulu ndi woyenera kwambiri kumutamanda;
Iyeyo ayenera kuopedwa kuposa milungu yonse.
26 Pakuti milungu yonse ya anthu a mitundu ina ndi mafano wopanda pake,
koma Yehova analenga kumwamba.
27 Ulemerero ndi ufumu zili pamaso pake;
mphamvu ndi chimwemwe zili pa malo pokhala Iye.
28 Perekani kwa Yehova, Inu mabanja a anthu a mitundu ina,
perekani kwa Yehova ulemerero ndi mphamvu,
29 perekani kwa Yehova ulemerero woyenera dzina lake.
Bweretsani chopereka ndipo mufike pamaso pake;
pembedzani Yehova mu ulemerero wachiyero chake.
30 Njenjemerani pamaso pake, dziko lonse lapansi!
Dziko linakhazikika kolimba; silingasunthidwe.
31 Zakumwamba zisangalale, dziko lapansi likondwere;
anene anthu a mitundu ina, "Yehova ndi mfumu!"
32 Nyanja ikokome, ndi zonse zili m'menemo;
minda ikondwere, ndi zonse zili m'menemo!
33 Ndipo mitengo ya m'nkhalango idzayimba,
idzayimba chifukwa cha chimwemwe pamaso pa Yehova,
pakuti akubwera kudzaweruza dziko lapansi.

34 Yamikani Yehova, pakuti Iye ndi wabwino;
chikondi chake chikhala mpaka muyaya.
35 Fuwulani kuti, "Tipulumutseni, Inu Mulungu wa chipulumutso chathu,
mutisonkhanitse ndipo mutipulumutse kwa anthu a mitundu ina,
kuti tiyamike dzina lanu loyera,
kuti tikutamandeni."
36 Atamandike Yehova Mulungu wa Israeli,
kuyambira muyaya mpaka muyaya.
Ndipo anthu onse anati, "Ameni" ndipo "Tikutamandani Yehova."

37 Ndipo Davide anasiya Asafu pamodzi ndi anzake kumene kunali
Bokosi la Chipangano la Yehova kuti azitumikira kumeneko nthawi zonse,
monga mwa zoyenera kuchita pa tsiku lililonse. 38 Iye anasiyanso Obedi-
Edomu pamodzi ndi anzake 68 kuti azitumikira nawo pamodzi. Obedi-
Edomu mwana wa Yedutuni ndi Hosa anali alonda a pa chipata.
39 Davide anasiya wansembe Zadoki ndi ansembe anzake ku chihema
cha Yehova ku malo achipembedzo ku Gibiyoni 40 kuti azipereka nsembe
zopsereza kwa Yehova pa guwa lansembe nthawi zonse mmawa ndi
madzulo, potsata zonse zimene zinalembedwa m'buku la malamulo a
Yehova, amene anawapereka kwa Aisraeli. 41 Anthuwo anali pamodzi
ndi Hemani ndi Yedutuni ndi onse amene anawasankha mowatchula
dzina kuti apereke mayamiko kwa Yehova, "pakuti chikondi chake ndi
chosatha." 42 Hemani ndi Yedutuni anali oyang'anira malipenga ndi
ziwaya ndiponso zipangizo zina zoyimbira nyimbo zachipembedzo. Ana
a Yedutuni anawayika kuti aziyang'anira pa chipata.
43 Kenaka anthu onse anachoka, aliyense kupita kwawo. Ndipo Davide
anabwerera ku nyumba kwake kukadalitsa banja lake.

# 17

*Lonjezo la Mulungu kwa Davide*

1 Davide atakhazikika m'nyumba yake yaufumu, anawuza mneneri
Natani kuti, "Ine pano ndikukhala m'nyumba yaufumu yomanga ndi
mitengo ya mkungudza, pomwe Bokosi la Chipangano la Yehova lili mu
tenti."
2 Natani anayankha Davide kuti, "Chitani chilichonse chimene chili mu
mtima mwanu, chifukwa Mulungu ali nanu."
3 Usiku umenewo mawu a Mulungu anafika kwa Natani, ndipo anati,
4 "Pita kamuwuze mtumiki wanga Davide kuti, 'Yehova akunena kuti,
sudzandimangira ndiwe nyumba yokhalamo.' 5 Ine sindinakhalepo
m'nyumba kuyambira tsiku limene ndinatulutsa Israeli m'dziko la
Igupto mpaka lero lino. Ndakhala ndikuyenda kuchoka m'tenti ina
kupita m'tenti ina, kuchoka malo ena kupita malo ena. 6 Konse ndakhala
ndikuyenda ndi Aisraeli onse, kodi ndinanenapo kwa wina aliyense
wa atsogoleri awo amene ndinamulamula kuweta anthu anga kuti,
'Kodi n'chifukwa chiyani simunandimangire nyumba ya mitengo ya
mkungudza?' "
7 Ndipo tsopano umuwuze mtumiki wanga Davide kuti, "Yehova
Wamphamvuzonse akuti, Ine ndinakutenga ku busa ukuweta nkhosa,
kuti ukhale mtsogoleri wa anthu anga, Aisraeli. 8 Ineyo ndinali nawe
kulikonse kumene unkapita, ndipo ndachotsa adani ako onse pamaso
pako. Tsopano ndidzakuza dzina lako kuti likhale m'gulu la mayina
a anthu otchuka kwambiri pa dziko lapansi. 9 Ndipo ndidzawapatsa
malo anthu anga, Aisraeli ndipo ndidzawadzala pamalo awoawo kuti
asadzavutitsidwenso. Anthu oyipa sadzawazunzanso monga ankachi-
tira poyamba paja; 10 monga akhala akuchitira kuchokera nthawi imene
ndinasankha atsogoleri a anthu anga Aisraeli. Ine ndidzagonjetsanso
adani anu onse.
" 'Ine ndikulengeza kwa iwe kuti Yehova adzakhazikitsa banja
lako. 11 Masiku ako akadzatha ndipo ukadzatsatira makolo ako, Ine
ndidzawutsa mphukira yako imene idzalowa m'malo mwako, mmodzi
mwa ana ako, ndipo ndidzakhazikitsa ufumu wake. 12 Iye ndiye

amene adzandimangira nyumba, ndipo ndidzakhazikitsa ufumu wake
kwamuyaya. 13 Ine ndidzakhala abambo ake, ndipo iye adzakhala
mwana wanga. Ine sindidzasiya kumukonda monga ndinachitira ndi
amene unalowa m'malo mwawo. 14 Ndidzamuyika kukhala wolamulira
nyumba yanga ndi ufumu wanga kwamuyaya. Mpando wake waufumu
udzakhazikika kwamuyaya.' "

15 Natani anafotokozera Davide mawu onse avumbulutso limene ana-
landira.

*Pemphero la Davide*

16 Choncho Mfumu Davide analowa mu tenti nakhala pamaso pa Yehova,
ndipo anati,

"Ine ndine yani, Inu Yehova Mulungu, ndipo banja langa n'chiyani
kuti mundifikitse pamene ndafikapa? 17 Inu Mulungu, kukhala ngati izi
ndi zosakwanira pamaso panu, Inuyo mwayankhula zatsogolo la banja
la mtumiki wanu. Mwandiyang'ana ndipo mwandiyesa ngati munthu
wolemekezeka kwambiri pakati pa anthu, Inu Yehova Mulungu."

18 "Kodi Davide anenenso chiyani kwa Inu, pakuti mwachitira ulemu
wotere mtumiki wanu? Pakuti Inu mukumudziwa mtumiki wanu. 19 Inu
Yehova, chifukwa cha mtumiki wanu komanso mwa chifuniro chanu,
mwachita chinthu chachikulu ichi ndipo mwawulula malonjezo anu
aakulu onse.

20 "Palibe wina wofanana nanu, Inu Yehova, ndipo palibe Mulungu
wina koma Inu nokha monga tamvera ndi makutu athu. 21 Ndipo
ndi ndani wofanana ndi anthu anu Aisraeli, mtundu wokhawo pa
dziko lapansi umene Mulungu wake anapita kukawuwombola, monga
anthu akeake ndi kukadzitchukitsa yekha pochita zinthu zodabwitsa
zazikulu, pothamangitsa mitundu ina pamaso pa anthu ake, amene Inu
munawawombola ku Igupto? 22 Inu munawapanga anthu anu Aisraeli
kukhala anuanu kwamuyaya, ndipo Inu, Inu Yehova ndinu Mulungu
wawo.

23 "Ndipo tsopano Yehova, sungani kwamuyaya lonjezo limene mwa-
chita ndi mtumiki wanu ndi banja lake, likhazikitseni kwamuyaya.
Chitani monga mwalonjezera, 24 kotero dzina lanu likhazikike ndi
kukhala lotchuka mpaka muyaya. Ndipo anthu adzanena kuti, 'Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa woyang'anira Israeli, ndi Mulungu wa
Israeli!' Ndipo banja la mtumiki wanu Davide lidzakhazikika pamaso
panu.

25 "Inu Mulungu wanga, mwaululira mtumiki wanu kuti mudza-
mumangira nyumba. N'chifukwa chake ine mtumiki wanu ndalimba
mtima kupemphera motere. 26 Inu Yehova, ndinu Mulungu! Mwalon-
jeza zinthu zabwinozi kwa mtumiki wanu. 27 Ndipo chakukomerani
kudalitsa banja la mtumiki wanu kuti likhale pamaso panu mpaka
muyaya. Pakuti Inu Yehova mwalidalitsa, lidzakhala lodalitsika mpaka
muyaya."

# 18

*Nkhondo za Davide ndi Kupambana Kwake*

1 Patapita nthawi, Davide anagonjetsa Afilisti ndipo anakhala pansi pa
ulamuliro wake. Iye analanda Gati ndi midzi yake yozungulira m'manja
mwa Afilistiwo.

2 Davide anagonjetsanso Amowabu, nakhala pansi pa ulamuliro wake
ndipo ankapereka msonkho kwa iye.
3 Komanso Davide anagonjetsa Hadadezeri mfumu ya Zoba, mpaka ku
Hamati, pamene anapita kukakhazikitsa ulamuliro wake m'mbali mwa
mtsinje wa Yufurate. 4 Davide analanda magaleta 1,000, anthu okwera
magaleta 7,000 pamodzi ndi asilikali oyenda pansi 20,000. Iye anadula
mitsempha ya akavalo onse okoka magaleta, koma anasiyapo akavalo 100
okha.
5 Aramu wa ku Damasiko atabwera kudzathandiza Hadadezeri mfumu
ya ku Zoba, Davide anakantha asilikali 22,000. 6 Iye anakhazikitsa
maboma mu ufumu wa Aramu wa ku Damasiko, ndipo Aaramu anakhala
pansi pa ulamuliro wake ndipo ankapereka msonkho. Yehova ankamu-
patsa chipambano Davide kulikonse kumene ankapita.
7 Davide anatenga zishango zagolide zimene ankanyamula akulu-
akulu ankhondo a Hadadezeri ndi kubwera nazo ku Yerusalemu.
8 Kuchokera ku Teba ndi Kuni, mizinda ya Hadadezeri, Davide anatengako
mkuwa wambiri umene Solomoni anapangira chimbiya, zipilala ndi zida
zosiyanasiyana zamkuwa.
9 Tou, mfumu ya Hamati atamva kuti Davide wagonjetsa gulu lonse
lankhondo la Hadadezeri mfumu ya Zoba, 10 anatumiza mwana wake
Hadoramu kwa mfumu Davide kukamulonjera ndi kukamuyamikira
chifukwa cha kupambana kwake pa nkhondo yake ndi Hadadezeriyo,
amene analinso pa nkhondo ndi Tou. Hadoramu anabweretsa ziwiya
zosiyanasiyana zagolide, zasiliva ndi zamkuwa.
11 Mfumu Davide inapereka zinthu zimenezi kwa Yehova, monga
anachitira ndi siliva ndi golide zochokera ku mayiko ena onse monga
Edomu ndi Mowabu, Aamoni ndi Afilisti, ndi Aamaleki.
12 Abisai mwana wa Zeruya anakantha Aedomu 18,000 mu Chigwa cha
Mchere. 13 Iye anayika maboma ku Edomu, ndipo Aedomu onse anakhala
pansi pa Davide. Yehova ankapambanitsa Davide kulikonse kumene
ankapita.

### *Akuluakulu a Davide*

14 Davide analamulira dziko lonse la Israeli ndipo ankachita zonse
mwachilungamo ndi molondola pamaso pa anthu ake onse. 15 Yowabu,
mwana wa Zeruya anali mkulu wa ankhondo; Yehosafati mwana wa
Ahiludi anali mlembi wa zochitika; 16 Zadoki, mwana wa Ahitubi ndi
Ahimeleki mwana wa Abiatara anali ansembe; Savisa anali mlembi;
17 Benaya mwana wa Yehoyada anali mtsogoleri wa Akereti ndi Apeleti,
ndipo ana a Davide anali alangizi a mfumu.

## 19

### *Davide Achita Nkhondo ndi Aamoni*

1 Patapita nthawi Nahasi mfumu ya Aamoni inamwalira, ndipo mwana
wake analowa ufumu m'malo mwake. 2 Davide anaganiza kuti, "Ine
ndidzachitira chifundo Hanuni mwana wa Nahasi chifukwa abambo
ake anandichitira zabwino." Choncho Davide anatumiza anthu kuti
akamupepesere kwa Hanuni chifukwa cha imfa ya abambo ake.
Anthu amene Davide anawatuma atafika kwa Hanuni m'dziko la
Aamoni kudzamupepesa, 3 atsogoleri a ankhondo a Aamoni anawuza
Hanuni kuti, "Kodi mukuganiza kuti Davide akupereka ulemu kwa
abambo anu potumiza anthuwa kwa inu kudzapepesa? Kodi anthuwa

sanawatumize kuti adzaone dziko lathu ndi kuchita ukazitape ndi cholinga
chofuna kuwulanda?” 4 Choncho Hanuni anagwira anthu amene Da-
vide anawatuma aja ndipo anawameta ndi kudula zovala zawo pakati
m’chiwuno mpaka matako kuonekera ndipo anawabweza kwawo.

5 Munthu wina atafika ndi kufotokozera Davide za anthuwo, iye
anatuma amithenga kukakumana nawo, chifukwa anali ndi manyazi
kwambiri. Mfumu inati, “Mukhale ku Yeriko mpaka ndevu zanu zitakula,
ndipo kenaka mubwere kuno.”

6 Aamoni atazindikira kuti amukwiyitsa kwambiri Davide, Hanuni ndi
Aamoni anatumiza siliva wolemera makilogalamu 34,000 kuti akalipirire
magaleta ndi okwerapo ake a ku Mesopotamiya; Aramu-Maaka ndi Zoba.
7 Iwo analipira magaleta okwanira 32,000, pamodzi ndi mfumu ya ku
Maaka ndi ankhondo ake. Amenewa anabwera ndi kudzamanga misasa
yawo pafupi ndi Medeba. Nawonso Aamoni anabwera kuchokera ku
mizinda yawo ndipo anapita kukachita nkhondo.

8 Davide atamva zimenezi, anatumiza Yowabu ndi gulu lonse la
ankhondo amphamvu. 9 Aamoni anatuluka ndi kukhala m’mizere ya
nkhondo pa chipata cha mzinda wawo, pamene mafumu amene anabwera
nawo anali kwa wokha, ku malo wopanda mitengo.

10 Yowabu ataona kuti kunali mizere ya ankhondo kutsogolo kwake ndi
kumbuyo kwake; iye anasankha ena mwa ankhondo a Israeli odziwa
kuchita bwino nkhondo ndipo anawayika kuti amenyane ndi Aaramu.
11 Iye anayika ankhondo ena otsalawo m’manja mwa Abisai m’bale
wake ndipo anawayika kuti amenyane ndi Aamoni. 12 Yowabu anati,
“Ngati Aaramu andipose mphamvu, iwe ubwere udzandipulumutse; koma
ngati Aamoni akupose mphamvu, ine ndidzabwera kudzakupulumutsa.
13 Limba mtima ndipo timenyane nawo mopanda mantha chifukwa cha
anthu athu ndi mizinda ya Mulungu wathu. Yehova achite chomukomera
pamaso pake.”

14 Choncho Yowabu ndi ankhondo amene anali naye anapita kuka-
menyana ndi Aaramu, ndipo iwo anathawa pamaso pake. 15 Aamoni
atazindikira kuti Aaramu akuthawa, iwo anathawanso pamaso pa Abisai
m’bale wake ndi kulowa mu mzinda. Motero Yowabu anabwerera ku
Yerusalemu.

16 Aaramu ataona kuti agonjetsedwa ndi Aisraeli, anatumiza amithenga
kukayitana Aaramu amene anali ku tsidya la Mtsinje, pamodzi ndi
mtsogoleri wa ankhondo wa Hadadezeri, Sofaki akuwatsogolera.

17 Davide atawuzidwa zimenezi, iye anasonkhanitsa Aisraeli onse
ndi kuwoloka Yorodani. Iyeyo anapita kukakumana nawo ndipo
anakhala m’mizere yankhondo moyang’anana ndipo iwo anamenyana
naye. 18 Koma iwo anathawa pamaso pa Aisraeli, ndipo Davide anapha
anthu okwera pa magaleta 7,000 ndi ankhondo oyenda pansi 40,000. Iye
anaphanso Sofaki, mtsogoleri wawo wankhondo.

19 Mafumu amene ali pansi pa Hadadezeri ataona kuti agonjetsedwa ndi
Aisraeli, anachita mtendere ndi Davide ndipo anakhala pansi pa ulamuliro
wake.

Motero Aaramu anaopa kuthandizanso Aamoni.

# 20

*Davide Alanda Raba*

1 Nthawi ya mphukira, nthawi imene mafumu amapita ku nkhondo,
Yowabu anatsogolera gulu la ankhondo. Iye anawononga Aamoni, kenaka
anapita ku mzinda wa Raba ndipo anawuzungulira, koma Davide anatsala
ku Yerusalemu. Yowabu anathira nkhondo mzinda wa Raba ndipo
anawuwononga. 2 Davide anachotsa chipewa chaufumu pamutu pa
mfumu yawo. Chipewacho chinkalemera makilogalamu asanu agolide
ndiponso chinali ndi miyala yokongola. Ndipo Davide anavala chipewa-
cho. Iye anatenga katundu wambiri kuchokera mu mzindawo, 3 ndipo
anatulutsa anthu amene anali m'menemo, nawayika kuti azigwira ntchito
ya macheka, yosula makasu ndi nkhwangwa. Davide anachita izi ndi
mizinda yonse ya Aamoni. Kenaka Davide pamodzi ndi gulu lake lonse
lankhondo anabwerera ku Yerusalemu.

### *Davide Achita Nkhondo ndi Afilisti*

4 Patapita nthawi, nkhondo inayambika pakati pa Aisraeli ndi Afilisti ku Gezeri. Nthawi imeneyo Sibekai Mhusati anapha Sipai, mmodzi mwa zidzukulu za Arefai, ndipo Afilisti anagonja.

5 Pa nkhondo inanso ndi Afilisti, Elihanani mwana wa Yairi anapha Lahimi m'bale wake wa Goliati Mgiti, amene mkondo wake unali ngati ndodo yowombera nsalu.

6 Pa nkhondo inanso imene inachitika ku Gati, panali munthu wina
wamtali kwambiri, wa zala zisanu ndi chimodzi m'manja ndi m'mapazi
ndipo zonse pamodzi zinalipo 24. Iyenso anali chidzukulu cha Rafa.
7 Pamene iye ankanyoza Aisraeli, Yonatani mwana wa Simea, m'bale wake
wa Davide anamupha.

8 Anthu amenewa anali zidzukulu za Rafa ku Gati, ndipo anaphedwa ndi Davide ndi ankhondo ake.

# 21

### *Davide Awerenga Ankhondo Ake*

1 Satana anafuna kuvutitsa Aisraeli choncho anawutsa mtima wa Davide
kuti awerenge Aisraeli. 2 Choncho Davide anati kwa Yowabu pamodzi
ndi atsogoleri a ankhondo, "Pitani mukawerenge Aisraeli kuyambira
ku Beeriseba mpaka ku Dani. Ndipo mudzandiwuze kuti ndidziwe
chiwerengero chawo."

3 Yowabu anayankha kuti, "Yehova achulukitse ankhondo ake kukhala miyandamiyanda. Mbuye wanga mfumu, kodi anthu onsewa sali pansi panu? N'chifukwa chiyani mbuye wanga mukufuna kuchita zimenezi? N'chifukwa chiyani mukufuna kuchimwitsa Israeli?"

4 Komabe mawu a mfumu anapambana mawu a Yowabu, kotero
Yowabu anapita mu Israeli monse ndipo kenaka anabwera ku Yerusalemu.
5 Yowabu anapereka chiwerengero cha anthu ankhondo kwa Davide:
Mu Israeli monse munali anthu ankhondo 1,100,000 amene amadziwa
kugwiritsa ntchito lupanga, kuphatikizapo anthu 470,000 a fuko la Yuda.

6 Koma Yowabu sanaphatikizepo fuko la Levi ndi fuko la Benjamini
pa chiwerengerochi, pakuti lamulo la mfumu linamuyipira. 7 Lamulo
limeneli silinakomerenso Mulungu. Kotero Iye analanga Israeli.

8 Choncho Davide anati kwa Mulungu, "Ine ndachimwa kwambiri pa zimene ndachita. Tsono ndikupempha kuti mukhululuke kulakwa kwa mtumiki wanu. Ine ndachita zopusa kwambiri."

9 Yehova anati kwa Gadi, mlosi wa Davide, 10 “Pita ukamuwuze Davide
kuti, ‘Yehova akuti, Ine ndikukupatsa zinthu zitatu izi. Usankhepo
chimodzi pa zimenezi choti ndikuchitire.’ ”

11 Choncho Gadi anapita kwa Davide ndipo anati kwa Iye, “Yehova akuti,
‘Musankhepo chimene mungakonde kuti chichitike: 12 m’dziko mukhale
njala zaka zitatu, mukhale mukuthawa adani anu kwa miyezi itatu,
akukukanthani ndi lupanga la Yehova, kapena m’dziko mukhale mliri kwa
masiku atatu, mngelo wa Yehova akuwononga Israeli yense.’ Ndipo tsono
ganizirani bwino chomwe ndikamuyankhe amene wandituma.”

13 Davide anati kwa Gadi, “Ine ndavutika kwambiri mu mtima
mwanga. Ine andilange ndi Yehova, pakuti chifundo chake ndi chachikulu
kwambiri; koma ndisalangidwe ndi anthu.”

14 Choncho Yehova anabweretsa mliri pa Aisraeli, ndipo unapha Aisraeli
70,000. 15 Ndipo Mulungu anatumiza mngelo kuti awononge Yerusalemu.
Koma pamene mngeloyo amachita zimenezi, Yehova anaona ndipo
anavutika mu mtima chifukwa cha zowawazo ndipo anati kwa mngelo
amene ankawononga anthu uja, “Basi kwakwanira! Leka kuwononga.”
Nthawi imeneyo mngelo wa Yehova anali atayima pamalo opunthira tirigu
a Arauna Myebusi.

16 Davide anakweza maso ake ndipo anaona mngelo wa Yehova atayima
pakati pa dziko lapansi ndi kumwamba, m’dzanja lake muli lupanga
lotambalitsa kuloza ku Yerusalemu. Ndipo Davide ndi akuluakulu, atavala
ziguduli, anadzigwetsa pansi chafufumimba.

17 Davide anati kwa Mulungu, “Kodi si ine amene ndinalamula kuti
ankhondo awerengedwe? Ine m’busa ndi amene ndachimwa, ndiye
ndachita zoyipa. Anthuwa ali ngati nkhosa zosalakwa. Kodi iwowa achita
chiyani? Inu Yehova Mulungu wanga, langani ineyo pamodzi ndi banja
langa, koma musalole kuti mliriwu ukhale pa anthu anuwa.”

18 Pamenepo mngelo wa Yehova analamula Gadi kuti awuze Davide kuti
akamange guwa lansembe la Yehova pamalo opunthira tirigu a Arauna
Myebusi. 19 Ndipo Davide anapita pomvera mawu amene Gadi ananena
m’dzina la Yehova.

20 Pamene Arauna ankapuntha tirigu, anatembenuka ndipo anaona
mngelo ndipo ana ake anayi aamuna amene anali naye anabisala.
21 Davide anayandikira, ndipo Arauna atayang’ana ndi kumuona, ana-
choka popunthira tirigupo ndipo anawerama nagunditsa nkhope yake
pansi pamaso pa Davide.

22 Davide anati kwa Arauna, “Undipatse malo ako opunthira tirigu kuti
ndimangire Yehova guwa lansembe, kuti mliri uli pa anthuwa usiye.
Undigulitse ine pa mtengo woyenera ndithu.”

23 Arauna anati kwa Davide, “Tengani! Mbuye wanga mfumu achite
chomukomera. Taonani ine ndidzapereka ng’ombe zazimuna za nsembe
yopsereza, zopunthira tirigu zidzakhala nkhuni ndipo tiriguyu adzakhala
chopereka chachakudya. Ndidzapereka zonsezi.”

24 Koma mfumu Davide inayankha Arauna kuti, “Ayi, ine ndikuti
ndipereka mtengo wathunthu. Sindingatenge chinthu chako ndi
kuchipereka kwa Yehova, kapena kupereka nsembe imene sindinayigule.”

25 Choncho Davide analipira Arauna masekeli agolide 600 chifukwa
cha malowo. 26 Davide anamangira Yehova guwa lansembe pamenepo
ndipo anaperekapo nsembe zopsereza ndi nsembe zachiyanjano. Iye
anapemphera kwa Yehova, ndipo Yehova anayankha potumiza moto pa
guwa lansembe zopsereza kuchokera kumwamba.

[27] Tsono Yehova anayankhula kwa mngelo, ndipo analowetsa lupanga
lake m'chimake. [28] Pa nthawi imeneyo, Davide ataona kuti Yehova
wamuyankha pa malo opunthira tirigu a Arauna Myebusi, anapereka
nsembe pamenepo. [29] Tenti ya Yehova imene Mose anapanga m'chipululu,
ndi guwa lansembe zopsereza pa nthawi imeneyi zinali pa phiri ku
Gibiyoni. [30] Koma Davide sanathe kupita kumeneko kuti akapemphere
pamaso pa Yehova, chifukwa amaopa lupanga la mngelo wa Yehova.

# 22

[1] Ndipo Davide anati, “Nyumba ya Yehova Mulungu idzakhala pano,
ndiponso guwa lansembe zopsereza za Israeli.”

### *Kukonzekera Kumanga Nyumba ya Mulungu*

[2] Choncho Davide analamula kuti asonkhanitse alendo onse amene
amakhala mu Israeli ndipo kuchokera pakati pawo anasankha amisiri
a miyala kuti aseme miyala yomangira nyumba ya Mulungu. [3] Ndipo
anapereka zitsulo zambiri zopangira misomali ya zitseko za pa zipata ndi
zolumikiza zake. Anaperekanso mkuwa wochuluka wokanika kuwuyeza.
[4] Iye anaperekanso mitengo yambiri ya mkungudza, yosawerengeka,
pakuti anthu a ku Sidoni ndi a ku Turo anabweretsa yambiri kwa Davide.
[5] Davide anati, “Mwana wanga Solomoni ndi wamng'ono ndipo sadziwa
zambiri. Koma nyumba yomwe timangire Yehova iyenera kukhala
yaulemerero, yotchuka ndi yokongola pamaso pa anthu a mitundu
yonse. Choncho ndikonzekeratu zambiri.” Motero Davide anayikonzekera
kwambiri asanamwalire.
[6] Tsono iye anayitana Solomoni mwana wake ndipo anamulamula kuti
adzamangire nyumba Yehova Mulungu wa Israeli. [7] Davide anati kwa
Solomoni, “Mwana wanga, ine ndinali ndi maganizo oti ndimangire
nyumba Dzina la Yehova Mulungu wanga. [8] Koma Yehova anandiyankhula
kuti, ‘Iwe wapha anthu ambiri ndiponso wachita nkhondo zambiri.
Sumangira dzina langa nyumba chifukwa wapha anthu ambiri pa
dziko lapansi pamaso panga. [9] Koma udzabala mwana wamwamuna
amene adzakhala munthu wamtendere ndi wabata ndipo ndidzamupatsa
mpumulo kuchokera kwa adani ake onse a mbali zonse. Dzina lake
adzatchedwa Solomoni ndipo Ine ndidzapereka mtendere ndi bata kwa
Israeli pa nthawi ya ulamuliro wake. [10] Iye ndiye adzandimangire
nyumba. Adzakhala mwana wanga ndipo Ine ndidzakhala abambo ake.
Ndipo ndidzakhazikitsa mpando wake waufumu m'dziko la Israeli mpaka
muyaya.’ ”
[11] “Tsopano mwana wanga, Yehova akhale nawe ndipo upambane
ndi kumanga Nyumba ya Yehova Mulungu wako, monga momwe Iye
ananenera kuti udzatero. [12] Yehova akupatse nzeru ndi kumvetsetsa
pamene Iye adzakuyika kukhala wolamulira Israeli, kuti udzasunge
malamulo a Yehova Mulungu wako. [13] Ndipo udzapambana ngati
udzamvera mosamala malangizo ndi malamulo amene Yehova anapereka
kwa Aisraeli kudzera mwa Mose. Khala wamphamvu ndi wolimba mtima.
Usachite mantha kapena kutaya mtima.
[14] “Ine movutikira kwambiri ndapereka ku Nyumba ya Mulungu matani
3,400 agolide, matani 34,000 asiliva, ndiponso mkuwa ndi chitsulo,
matabwa ndi miyala. Ndipo iwe utha kuwonjezerapo pa zimenezi.
[15] Iwe uli ndi antchito ambiri: osema miyala, amisiri a miyala, ndi
amisiri a matabwa, komanso anthu ambiri aluso la ntchito zosiyanasiyana,

16 zagolide ndi zasiliva, zamkuwa, zazitsulo, amisiri osawerengeka.
Tsopano yamba ntchito, ndipo Yehova akhale nawe."

17 Tsono Davide analamula atsogoleri onse a Israeli kuti athandize
Solomoni mwana wake. 18 Iye anawawuza kuti, "Kodi Yehova Mulungu,
sali nanu? Ndipo Iye siwakupatsani mpumulo mbali zonse? Pakuti Iyeyo
wapereka eni nthaka kwa inu ndipo dziko lili pa ulamuliro wa Yehova ndi
anthu ake. 19 Tsono perekani mtima wanu ndi moyo wanu kufunafuna
Yehova Mulungu wanu. Yambani kumanga malo opatulika a Yehova
Mulungu, kuti mubweretse Bokosi la Chipangano la Yehova ndi zinthu
zopatulika za Mulungu m'Nyumba ya Mulungu imene idzamangidwa
chifukwa cha dzina la Yehova."

# 23

*Fuko la Levi*

1 Davide atakalamba, ali ndi zaka zambiri, anayika Solomoni mwana
wake kukhala mfumu ya Israeli.

2 Iye anasonkhanitsanso pamodzi atsogoleri onse a Israeli, pamodzi
ndi ansembe ndi Alevi. 3 Anawerenga Alevi kuyambira a zaka makumi
atatu ndi kupitirirapo, ndipo chiwerengero cha amuna onse chinali 38,000.
4 Davide anati, "Mwa amenewa, amuna 24,000 aziyang'anira ntchito za
m'Nyumba ya Mulungu ndipo 6,000 akhale akuluakulu ndi oweruza.
5 Amuna 4,000 akhale alonda a pa zipata ndipo 4,000 azitamanda Yehova
ndi zipangizo zoyimbira zimene ndazipereka ndi cholinga chimenecho."

6 Davide anagawa Aleviwo m'magulumagulu motsatira ana a Levi awa:
Geresoni, Kohati ndi Merari.

*Banja la Geresoni*

7 Ana a Geresoni:
Ladani ndi Simei.
8 Ana a Ladani:
Mtsogoleri Yehieli, Zetamu ndi Yoweli. Onse analipo atatu.
9 Ana a Simei:
Selomoti, Haziyeli ndi Harani. Onse analipo atatu.
Awa anali atsogoleri a mabanja a Ladani.
10 Ndipo ana a Simei anali:
Yahati, Zina, Yeusi ndi Beriya.
Awa anali ana a Semei. Onse analipo anayi.
11 Mtsogoleri anali Yahati, ndipo Ziza anali wachiwiri, koma Yeusi ndi
Beriya analibe ana aamuna ambiri. Kotero iwo anawerengedwa
ngati banja limodzi ndipo anapatsidwa ntchito imodzinso yofanana.

*Banja la Kohati*

12 Ana a Kohati:
Amramu, Izihari, Hebroni ndi Uzieli. Onse analipo anayi.
13 Ana a Amramu:
Aaroni ndi Mose.
Aaroni ndi zidzukulu zake anapatulidwa kwamuyaya kuti azipereka
zinthu zopatulika kwambiri monga nsembe pamaso pa Yehova,
komanso kuti azitumikira pamaso pake ndi kumadalitsa anthu
m'dzina lake kwamuyaya. 14 Ana a Mose munthu wa Mulungu
anawerengedwa ngati gawo la fuko la Levi.

15 Ana a Mose:
Geresomu ndi Eliezara.
16 Zidzukulu za Geresomu:
Mtsogoleri anali Subaeli.
17 Zidzukulu za Eliezara:
Mtsogoleri anali Rehabiya.
Eliezara analibe ana ena aamuna, koma ana a Rehabiya anali ochuluka kwambiri.
18 Ana a Izihari:
Mtsogoleri anali Selomiti.
19 Ana a Hebroni:
Mtsogoleri anali Yeriya, wachiwiri anali Amariya, Yahazieli anali wachitatu ndipo Yekameamu anali wachinayi.
20 Ana a Uzieli:
Mtsogoleri anali Mika ndipo wachiwiri anali Isiya.

*Banja la Merari*

21 Ana a Merari:
Mahili ndi Musi.
Ana a Mahili:
Eliezara ndi Kisi.
22 Eliezara anamwalira wopanda ana aamuna. Iye anali ndi ana
aakazi okhaokha. Abale awo, ana a Kisi, ndiwo amene anawakwatira.
23 Ana a Musi:
Mahili, Ederi ndi Yeremoti. Onse analipo atatu.

24 Izi zinali zidzukulu za Levi mwa mabanja awo, atsogoleri a mabanja
monga momwe analembedwera mayina awo ndi monga momwenso
anawerengedwera, banja lililonse pa lokha. Awa ndi anthu ogwira ntchito
oyambira zaka makumi awiri zobadwa kapena kupitirirapo, amene
amatumikira m'Nyumba ya Yehova. 25 Popeza Davide anati, "Pakuti
Yehova Mulungu wa Israeli, wapereka mpumulo kwa anthu ake ndipo
wabwera kudzakhala mu Yerusalemu kwamuyaya, 26 sikofunikiranso kuti
Alevi azinyamula tenti kapena zipangizo za chipembedzo." 27 Potsata
malangizo otsiriza a Davide, Alevi anawerengedwa kuyambira amuna a
zaka makumi awiri zakubadwa kapena kupitirirapo.

28 Ntchito ya Alevi inali kuthandiza zidzukulu za Aaroni pa ntchito
yotumikira m'Nyumba ya Yehova monga kuyang'anira mabwalo, zipinda
zam'mbali, kuyeretsa zinthu zonse zachipembedzo, ndiponso kuchita
ntchito zina za m'nyumba ya Mulungu. 29 Iwo amayang'anira buledi
amene amayikidwa pa tebulo, ufa wa nsembe yachakudya, timitanda ta
buledi wopanda yisiti: kuphika ndi kusakaniza, ndiponso miyeso yonse
ndi kukula kwake. 30 Iwo amayimiriranso mmawa uliwonse kuthokoza
ndi kutamanda Yehova. Amachitanso chomwecho madzulo, 31 ndiponso
popereka nsembe zopsereza kwa Yehova pa Sabata ndi pa chikondwerero
cha Mwezi Watsopano, ndi pa nthawi yosankhidwa ya Chikondwerero.
Iwo amatumikira pamaso pa Yehova nthawi zonse mwa chiwerengero
chawo ndi momwe analangizidwira.

32 Ndipo kotero Alevi anachita ntchito yawo ya ku tenti ya msonkhano
ya ku Malo Opatulika ndiponso molamulidwa ndi abale awo, zidzukulu za
Aaroni, pa ntchito ya m'Nyumba ya Yehova.

# 24

*Magulu a Ansembe*

1 Magulu a ana a Aaroni anali awa:

Ana a Aaroni anali Nadabu, Abihu, Eliezara ndi Itamara. 2 Koma Nadabu
ndi Abihu anamwalira abambo awo asanamwalire, ndipo analibe ana
aamuna. Kotero Eliezara ndi Itamara ankatumikira monga ansembe.
3 Mothandizidwa ndi Zadoki chidzukulu cha Eliezara ndi Ahimeleki
chidzukulu cha Itamara, Davide anawagawa m'magulu molingana ndi
ntchito yawo yotumikira. 4 Atsogoleri ambiri anapezeka pakati pa
zidzukulu za Eliezara kusiyana ndi zidzukulu za Itamara ndipo anagaw-
idwa moyenera: atsogoleri 16 a mabanja ochokera kwa Eliezara, ndipo
atsogoleri asanu ndi atatu a mabanja ochokera kwa zidzukulu za Itamara.
5 Anawagawa mosakondera pochita maere, pakuti iwo anali akuluakulu
a ku malo opatulika ndi akuluakulu a Mulungu pakati pa zidzukulu za
Eliezara ndi Itamara.

6 Mlembi Semaya mwana wa Netaneli, Mlevi, analemba mayina awo pamaso pa mfumu ndi akuluakulu ake: wansembe Zadoki, Ahimeleki mwana wa Abiatara ndi atsogoleri a mabanja a ansembe ndiponso Alevi, banja limodzi kuchokera kwa Eliezara kenaka limodzi kuchokera kwa Itamara.

7 Maere woyamba anagwera Yehoyaribu,
achiwiri anagwera Yedaya,
8 achitatu anagwera Harimu,
achinayi anagwera Seorimu,
9 achisanu anagwera Malikiya,
achisanu ndi chimodzi anagwera Miyamini,
10 achisanu ndi chiwiri anagwera Hakozi,
achisanu ndi chitatu anagwera Abiya,
11 achisanu ndi chinayi anagwera Yesuwa,
a khumi anagwera Sekaniya,
12 a 11 anagwera Eliyasibu,
a 12 anagwera Yakimu,
13 a 13 anagwera Hupa,
a 14 anagwera Yesebeabu,
14 a 15 anagwera Biliga,
a 16 anagwera Imeri,
15 a 17 anagwera Heziri,
a 18 anagwera Hapizezi,
16 a 19 anagwera Petahiya,
a 20 anagwera Ezekieli,
17 a 21 anagwera Yakini,
a 22 anagwera Gamuli,
18 a 23 anagwera Delaya,
ndipo a 24 anagwera Maaziya.

19 Umu ndi mmene anasankhidwira kuti azigwira ntchito yotumikira pamene alowa m'Nyumba ya Yehova, motsatira dongosolo limene anapatsidwa ndi kholo lawo Aaroni, monga momwe Yehova Mulungu wa Israeli anamulamulira.

*Alevi Ena Onse*

20 Za zidzukulu zina zonse za Levi:
Kuchokera kwa ana a Amramu: Subaeli;
kuchokera kwa ana a Subaeli: Yehideya.
21 Kwa Rehabiya, kuchokera kwa ana ake:
Mtsogoleri anali Isiya.
22 Kuchokera ku banja la Izihari: Selomoti;
kuchokera kwa ana a Selomoti: Yahati.
23 Ana a Hebroni: woyamba anali Yeriya, wachiwiri anali Amariya, wachitatu anali Yahazieli ndipo Yekameamu anali wachinayi.
24 Mwana wa Uzieli: Mika;
kuchokera kwa ana a Mika: Samiri.
25 M'bale wa Mika: Isiya;
kuchokera kwa ana a Isiya: Zekariya.
26 Ana a Merari: Mahili ndi Musi.
Mwana wa Yaaziya: Beno.
27 Ana a Merari:
Kuchokera kwa Yaaziya: Beno, Sohamu, Zakuri ndi Ibiri.
28 Kuchokera kwa Mahili: Eliezara, amene analibe ana aamuna.
29 Kuchokera kwa Kisi:
Mwana wa Kisi: Yerahimeeli.
30 Ndipo ana a Musi: Mahili, Ederi ndi Yerimoti.

Awa anali Alevi potsata mabanja a makolo awo. 31 Iwonso anachita
maere, monga anachitira abale awo, zidzukulu za Aaroni, pamaso pa
mfumu Davide, ndi Zadoki ndi Ahimeleki, atsogoleri a mabanja a ansembe
ndi Alevi. Mabanja a mwana wamkulu anachita nawo mofanana ndi a
mwana wamng'ono.

# 25

*Anthu Oyimba Nyimbo*

1 Davide ndi atsogoleri a asilikali anapatula ena mwa ana a Asafu,
Hemani ndi Yedutuni ku utumiki wa uneneri pogwiritsa ntchito apangwe,
azeze ndi ziwaya zamalipenga. Tsopano nawu mndandanda wa anthu
amene ankagwira ntchito imeneyi:

2 Kuchokera kwa ana a Asafu:
Zakuri, Yosefe, Netaniya ndi Asareli. Ana a Asafu amalamulidwa ndi Asafu ndipo amanenera moyang'aniridwa ndi mfumu.
3 Kwa Yedutuni, kuchokera kwa ana ake:
Gedaliya, Zeri, Yesaya, Simei, Hasabiya ndi Matitiya. Onse analipo 9 ndipo amayang'aniridwa ndi Yedutuni abambo awo, amene amanenera pogwiritsa ntchito apangwe poyamika ndi kutamanda Yehova.
4 Kwa Hemani, kuchokera kwa ana ake:
Bukiya, Mataniya, Uzieli, Subaeli ndi Yerimoti; Hananiya, Hanani, Eliata, Gidaliti ndi Romamiti-Ezeri; Yosibakasa, Maloti, Hotiri ndi Mahazioti.
5 Onsewa anali ana a Hemani mlosi wa mfumu. Iye anapatsidwa anawa potsata mawu a Mulungu akuti adzamukweza. Mulungu anapatsa Hemani ana aamuna 14 ndi ana aakazi atatu.

6 Anthu onsewa ankayang'aniridwa ndi makolo awo pa mayimbidwe
a m'Nyumba ya Yehova. Iwowatu ankayimba ndi ziwaya zamalipenga,

azeze ndi apangwe potumikira m'Nyumba ya Mulungu. Koma Asafu,
Yedutuni ndi Hemani amayang'aniridwa ndi mfumu. 7 Iwo pamodzi ndi
abale awo onse ophunzitsidwa ndi aluso loyimbira Yehova chiwerengero
chawo chinali 288. 8 Ang'onoang'ono ndi akulu omwe, mphunzitsi ndi
wophunzira yemwe anachita maere pa ntchito zawo.

| | |
|---|---|
| 9 Maere woyamba amene anali a Asafu, anagwera Yosefe, | |
| ana ndi abale ake. | 12 |
| Maere achiwiri anagwera Gedaliya, | |
| ndi abale ake ndi ana ake. | 12 |
| 10 Maere achitatu anagwera Zakuri, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 11 Maere achinayi anagwera Iziri, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 12 Maere achisanu anagwera Netaniya, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 13 Maere achisanu ndi chimodzi anagwera Bukiya, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 14 Maere achisanu ndi chiwiri anagwera Yesarela, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 15 Maere achisanu ndi chitatu anagwera Yeshaya, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 16 Maere achisanu ndi chinayi anagwera Mataniya, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 17 Maere a khumi anagwera Simei, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 18 Maere a 11 anagwera Azareli, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 19 Maere a 12 anagwera Hasabiya, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 20 Maere a 13 anagwera Subaeli, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 21 Maere a 14 anagwera Matitiya, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 22 Maere a 15 anagwera Yeremoti, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 23 Maere a 16 anagwera Hananiya, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 24 Maere a 17 anagwera Yosibakasa, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 25 Maere a 18 anagwera Hanani, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 26 Maere a 19 anagwera Maloti, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 27 Maere a 20 anagwera Eliyata, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 28 Maere a 21 anagwera Hotiri, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 29 Maere a 22 anagwera Gidaliti, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 30 Maere a 23 anagwera Mahazioti, | |
| ana ake ndi abale ake. | 12 |
| 31 Maere a 24 anagwera Romamiti-Ezeri, | |
| ana ake ndi abale ake | 12. |

# 26

*Alonda a pa Zipata*

1 Magulu a alonda a pa zipata:

Kuchokera ku banja la Kora: Meselemiya mwana wa Kore, mmodzi mwa ana a Asafu.
2 Meselemiya anali ndi ana awa:
woyamba Zekariya,
wachiwiri Yediaeli,
wachitatu Zebadiya,
wachinayi Yatinieli,
3 wachisanu Elamu,
wachisanu ndi chimodzi Yehohanani,
ndipo wachisanu ndi chiwiri Elihunai.
4 Obedi-Edomu analinso ndi ana awa:
woyamba Semaya,
wachiwiri Yehozabadi,
wachitatu Yowa,
wachinayi Sakara,
wachisanu Netaneli,
5 wachisanu ndi chimodzi Amieli,
wachisanu ndi chiwiri Isakara
ndipo wachisanu ndi chitatu Peuletayi.
(Pakuti Mulungu anadalitsa Obedi-Edomu).

6 Mwana wake Semaya analinso ndi ana amene anali atsogoleri m'banja
la abambo awo chifukwa anali anthu amphamvu. 7 Ana a Semaya
anali: Otini, Refaeli, Obedi ndi Elizabadi; abale ake, Elihu ndi
Semakiya, analinso anthu amphamvu. 8 Onsewa anali adzukulu a
Obedi-Edomu. Iwo ndi ana awo ndiponso abale awo anali anthu aluso ndi amphamvu pogwira ntchito. Zidzukulu zonse za Obedi-Edomu zinalipo 62.
9 Meselemiya anali ndi ana ndi abale ake amene anali aluso ndipo onse analipo 18.

10 Hosa Mmerari anali ndi ana awa: woyamba anali Simiri (ngakhale
kuti iye sanali woyamba kubadwa, abambo ake anamusankha kuti
akhale mtsogoleri), 11 wachiwiri Hilikiya, wachitatu Tebaliya ndipo
wachinayi Zekariya. Ana ndi abale onse a Hosa analipo 13.
12 Magulu amenewa a alonda a pa zipata, motsogozedwa ndi atsogoleri
awo, anali ndi ntchito yotumikira m'Nyumba ya Yehova, monga momwe
amachitira abale awo. 13 Iwo anachita maere mwa mabanja awo aang'ono
ndi aakulu omwe kuti apeze mlonda pa chipata chilichonse.
14 Maere a chipata chakummwa anagwera Selemiya. Maere anachitikanso chifukwa cha mwana wake Zekariya, phungu wanzeru ndipo
maere a chipata chakumpoto anagwera iye. 15 Maere a chipata
chakummwera anagwera Obedi-Edomu, ndipo maere a nyumba yosungiramo katundu anagwera ana ake. 16 Maere a chipata chakumadzulo ndi
chipata cha Saleketi ku msewu wa ku mtunda anagwera Supimu ndi Hosa.
Mlonda ankayang'anana ndi mlonda mnzake: 17 Mbali ya kummawa
kunkakhala Alevi 6 pa tsiku, kumpoto anayi pa tsiku, kummwera anayi pa
tsiku ndipo awiri ankakhala pa nyumba yosungiramo katundu. 18 Ndipo

ku bwalo cha kumadzulo, anayi amakhala mu msewu ndi awiri pabwalo penipeni.

19 Awa anali magulu a alonda a pa zipata amene anali zidzukulu za Kora ndi Merari.

*Asungichuma ndi Akuluakulu Ena*

20 Abale awo Alevi, motsogozedwa ndi Ahiya, anali oyang'anira chuma cha nyumba ya Mulungu ndi zinthu zoperekedwa kwa Mulungu.

21 Adzukulu a Ladani, mmodzi mwa ana a Geresoni, amene anali
atsogoleri a mabanja a Ageresoni, anali awa: Yehieli, 22 ana a Yehieli,
Zetamu ndi m'bale wake Yoweli. Iwo amayang'anira chuma cha ku Nyumba ya Mulungu wa Yehova.

23 Kuchokera ku banja la Amramu, banja la Aizihara, banja la Ahebroni ndi banja la Auzieli:

24 Subaeli, chidzukulu cha Geresomu, mwana wa Mose, anali mkulu
woyang'anira chuma. 25 Abale ake obadwa mwa Eliezara, anali
Rekabiya mwana wake, Yesaya mwana wake, Yoramu mwana wake,
Zikiri mwana wake ndi Selomiti mwana wake. 26 Selomiti ndi
abale ake amayang'anira zinthu zonse zoperekedwa kwa Mulungu ndi mfumu Davide, atsogoleri a mabanja amene anali olamulira ankhondo 1,000, olamulira ankhondo 100, ndi olamulira ankhondo
ena. 27 Zina zofunkha ku nkhondo anazipereka kuti zikhale zokonzera
Nyumba ya Yehova. 28 Ndipo zonse zimene zinaperekedwa ndi Mlosi Samueli, Sauli mwana wa Kisi, Abineri mwana wa Neri ndiponso Yowabu mwana wa Zeruya ndi zinthu zonse zimene zinkaperekedwa zimasungidwa ndi Selomiti ndi abale ake.

29 Kuchokera ku banja la Izihari: Kenaniya ndi ana ake anapatsidwa ntchito kutali ndi Nyumba ya Mulungu ngati akuluakulu ndi oweruza Israeli.

30 Kuchokera ku banja la Ahebroni: Hasabiya ndi abale ake, anthu anzeru 1,700. Iwo ankayang'anira ntchito zonse za Yehova ndi ntchito
yonse ya mfumu cha kumadzulo kwa Yorodani. 31 Pa banja la
Ahebroni, Yeriya anali mtsogoleri monga mwa mbiri ya mibado ya mabanja awo. M'chaka cha 40 cha ufumu wa Davide, panachitika kafukufuku ndipo ena mwa anthu aluso a banja la Hebroni anapezeka
kuti anali ku Yazeri ku Giliyadi. 32 Yeriya anali ndi abale 2,700 amene
anali aluso ndiponso atsogoleri a mabanja. Mfumu Davide anawayika iwowa kuti aziyang'anira fuko la Rubeni, fuko la Gadi ndi theka la fuko la Manase pa zinthu zonse za Mulungu ndi za mfumu.

# 27

*Magulu a Anthu Ankhondo*

1 Uwu ndi mndandanda wa Aisraeli, atsogoleri a mabanja, olamulira asilikali 1,000, olamulira asilikali 100 ndi akuluakulu awo, amene ankatumikira mfumu m'zonse zokhudza magulu a ankhondo, amene amagwira ntchito mwezi ndi mwezi chaka chonse. Gulu lililonse linali ndi anthu 24,000.

2 Amene amalamulira gulu loyamba pa mwezi woyamba anali Yasobeamu mwana wa Zabidieli. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

3 Iyeyu anali chidzukulu cha Perezi ndipo anali mkulu wa atsogoleri onse a ankhondo mwezi woyamba.

4 Amene amalamulira gulu lachiwiri pa mwezi wachiwiri anali Dodai Mwahohi; Mikiloti ndiye anali mtsogoleri wa gulu lake. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

5 Wolamulira ankhondo wachitatu, pa mwezi wachitatu anali Benaya,
mwana wa wansembe Yehoyada. Iye anali mtsogoleri ndipo pa
gulu lake panali ankhondo 24,000.
6 Uyu ndi Benaya uja amene
anali wamphamvu pa gulu la anthu makumi atatu ndipo ndiye
amatsogolera anthu makumi atatu aja. Mwana wake Amizabadi ndiye
amatsogolera gulu lake.

7 Wachinayi pa mwezi wachinayi anali Asaheli m'bale wake wa Yowabu; ndipo mwana wake Zebadiya ndiye analowa m'malo mwake. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

8 Wachisanu pa mwezi wachisanu anali Samihuti, mdzukulu wa Izira. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

9 Wa 6 pa mwezi wa 6 anali Ira mwana wa Ikesi wa ku Tekowa. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

10 Wa 7 pa mwezi wa 7 anali Helezi Mpeloni wa fuko la Efereimu. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

11 Wa 8 pa mwezi wa 8 anali Sibekai Mhusati, wa mbumba ya Zera. Pa gulu lake panali asilikali 24,000

12 Wa 9 pa mwezi wa 9 anali Abiezeri wa banja la Anatoti, wa fuko la Benjamini. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

13 Wa khumi pa mwezi wa khumi anali Mahazayi wa ku Netofa, wa mbumba ya Zera. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

14 Mtsogoleri wa 11, pa mwezi wa 11 anali Benaya wa ku Piratoni, wa fuko la Efereimu. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

15 Mtsogoleri wa 12, pa mwezi wa 12 anali Helidai Mnetofa, wa banja la Otanieli. Pa gulu lake panali asilikali 24,000.

### *Akuluakulu a Mafuko a Israeli*

16 Akuluakulu amene amatsogolera mafuko a Israeli ndi awa:

Mtsogoleri wa fuko la Rubeni: Eliezara mwana wa Zikiri;
mtsogoleri wa fuko la Simeoni: Sefatiya mwana wa Maaka;
17 mtsogoleri wa fuko la Levi: Hasabiya mwana wa Kemueli,
mtsogoleri wa banja la Aaroni: Zadoki;
18 mtsogoleri wa fuko la Yuda: Elihu, m'bale wake wa Davide;
mtsogoleri wa fuko la Isakara: Omuri mwana wa Mikayeli;
19 mtsogoleri wa fuko la Zebuloni: Isimaiya mwana wa Obadiya;
mtsogoleri wa fuko la Nafutali: Yerimoti mwana wa Azirieli;
20 mtsogoleri wa fuko la Efereimu: Hoseya mwana wa Azaziya;
mtsogoleri wa fuko la theka la Manase: Yoweli mwana wa Pedaya;
21 mtsogoleri wa fuko la theka la Manase limene linali ku Giliyadi: Ido mwana wa Zekariya;
mtsogoleri wa fuko la Benjamini: Yaasieli mwana wa Abineri;
22 mtsogoleri wa fuko la Dani: Azareli mwana wa Yerohamu.

Awa anali akuluakulu a mafuko a Israeli.

23 Davide sanawerenge amuna amene anali ndi zaka makumi awiri
kapena kucheperapo, chifukwa Yehova analonjeza kuti adzachulukitsa
Aisraeli ngati nyenyezi zamumlengalenga. 24 Yowabu mwana wa Zeruya
anayamba kuwerenga amuna koma sanamalize. Mkwiyo unagwera
Aisraeli chifukwa cha zimenezi ndipo chiwerengerochi sanachilowetse
m'buku la mbiri ya mfumu Davide.

*Anthu Oyang'anira Chuma cha Mfumu*

25 Azimaveti mwana wa Adieli ankayang'anira nyumba zosungiramo katundu wa mfumu.

Yonatani mwana wa Uziya ankayang'anira nyumba zosungiramo katundu wa maboma ozungulira, mizinda, midzi ndi malo olondera.

26 Eziri mwana wa Kelubi ankayang'anira anthu ogwira ntchito yolima ku munda.

27 Simei wa ku Rama ankayang'anira minda ya mpesa.

Zabidi wa ku Sifamu ankayang'anira mphesa ndi mosungiramo mwake.

28 Baala-Hanani wa ku Gederi ankayang'anira mitengo ya olivi ndi ya mikuyu ya ku Sefela.

Yowasi ankayang'anira mafuta a Olivi.

29 Sitirayi wa ku Saroni ankayang'anira ziweto zimene amaweta ku Saroni.

Safati mwana wa Adilayi ankayang'anira ng'ombe zakuzigwa.

30 Obili Mwismaeli ankayang'anira ngamira.

Yehideya Mmerenoti ankayang'anira abulu.

31 Yazizi Mhagiri akayang'anira nkhosa ndi mbuzi.

Onsewa anali akuluakulu oyang'anira chuma cha mfumu Davide.

32 Yonatani, malume wake wa Davide, anali phungu wake ndipo anali
munthu wanzeru komanso analinso mlembi. Yehieli mwana wa Hakimoni
ankasamalira ana a mfumu.

33 Ahitofele anali phungu wa mfumu.

Husai Mwariki anali bwenzi la mfumu. 34 Ahitofele atamwalira m'malo
mwake munalowa Yehoyada mwana wa Benaya ndi Abiatara.

Yowabu anali mtsogoleri wa gulu lankhondo la mfumu.

# 28

*Ndondomeko ya Kamangidwe ka Nyumba ya Mulungu*

1 Davide anayitana akuluakulu onse a Israeli kuti asonkhane ku Yerusalemu: akuluakulu a mafuko, olamulira magulu a ntchito ya mfumu, olamulira ankhondo 1,000, ndi olamulira ankhondo 100, ndiponso akuluakulu onse osunga katundu ndi ziweto za mfumu ndi ana ake, pamodzinso ndi akuluakulu a ku nyumba yaufumu, anthu amphamvu ndi asilikali onse olimba mtima.

2 Mfumu Davide inayimirira ndipo inati: "Tamverani abale anga ndi
anthu anga. Ine ndinali ndi maganizo omanga nyumba monga malo
okhalamo Bokosi la Chipangano la Yehova, malo oyikapo mapazi a
Mulungu wathu, ndipo ndinakonza ndondomeko yomangira nyumbayo."
3 Koma Mulungu anati kwa ine, "Usandimangire nyumba chifukwa ndiwe
munthu wankhondo ndipo wakhala ukukhetsa magazi."

4 "Komabe Yehova Mulungu wa Israeli anasankha ine pakati pa onse a
banja langa kukhala mfumu ya Israeli kwamuyaya. Iye anasankha Yuda

kukhala mtsogoleri, ndipo pa banja la Yuda anasankha banja langa. Pakati
pa ana aamuna a abambo anga, kunamukomera Iye kundikhazika mfumu
ya Aisraeli onse. 5 Pa ana anga ambiri onse amene Yehova wandipatsa,
Iye wasankha mwana wanga Solomoni kuti akhale pa mpando waufumu
wa ufumu wa Yehova kuti alamulire Israeli." 6 Yehova anati kwa ine,
"Solomoni mwana wako ndiye amene adzamanga nyumba yanga ndi
mabwalo anga, pakuti Ine ndamusankha kuti akhale mwana wanga
ndipo Ine ndidzakhala abambo ake. 7 Ine ndidzakhazikitsa ufumu wake
kwamuyaya ngati iye saleka kutsatira malamulo ndi malangizo anga,
monga momwe zikuchitikira leromu."

8 "Tsono lero ine ndikulamula inu pamaso pa Aisraeli onse ndi pa
msonkhano wa Yehova, ndipo Mulungu wathu akumva: Mutsatire
mosamala malamulo a Yehova Mulungu wathu, kuti dziko labwinoli
likhale lanu ndi kuti mudzalipereke kwa zidzukulu zanu kukhala cholowa
chawo kwamuyaya."

9 "Ndipo iwe mwana wanga Solomoni, umvere Mulungu wa abambo
ako, umutumikire ndi mtima wodzipereka kwathunthu ndi mtima wako
wonse, pakuti Yehova amasanthula mtima wa aliyense, ndipo amadziwa
maganizo aliwonse a munthu. Ngati ufunafuna Yehova, Iye adzapezeka;
koma ngati umutaya, Iye adzakukana kwamuyaya. 10 Tsopano ganizira
bwino, pakuti Yehova wakusankha iwe kuti umange Nyumba ya Mulungu
monga malo ake opatulika. Khala wamphamvu ndipo ugwire ntchito."

11 Kotero Davide anapatsa Solomoni mwana wake mapulani a khonde la
Nyumba ya Mulungu, nyumba zake, mosungiramo katundu, zipinda zake
zam'mwamba, zipinda zam'kati ndi malo a nsembe zopepesera machimo.
12 Iye anapatsa Solomoni mapulani a zonse zimene ankaziganizira za
bwalo la Nyumba ya Yehova ndi zipinda zonse zozungulira, zipinda
zosungiramo chuma cha Nyumba ya Mulungu ndi zinthu zoperekedwa
kwa Yehova. 13 Davide anamulangiza za magulu a ansembe ndi Alevi
ndi ntchito yonse yotumikira m'Nyumba ya Yehova, komanso za zinthu
zonse zogwirira ntchito potumikira. 14 Iye anakonzeratu za kulemera kwa
golide wopangira zida zonse zagolide zogwirira ntchito zosiyanasiyana,
ndiponso kulemera kwa siliva wopangira zida zonse zasiliva zogwirira
ntchito zosiyanasiyana: 15 kulemera kwa golide wopangira choyikapo
nyale chagolide ndi nyale zake; ndiponso kulemera kwa siliva wa
choyikapo nyale chilichonse ndi nyale zake, molingana ndi kagwiritsidwe
ka choyikapo nyale chilichonse; 16 kulemera kwa golide wa tebulo iliyonse
yoyikapo buledi wopatulika; kulemera kwa siliva wopangira matebulo
asiliva; 17 muyeso wa golide woyengeka bwino wopangira mafoloko,
mbale ndi zotungira; muyeso wa golide wa beseni lililonse la siliva;
18 ndiponso muyeso wa golide wabwino wopangira guwa la zofukiza.
Davide anamupatsanso ndondomeko ya mapangidwe a galeta, akerubi
agolide atatambasula mapiko awo kuphimba Bokosi la Chipangano la
Yehova.

19 Davide anati, "Zonsezi ndalemba kuchokera kwa Yehova, ndipo Iye
wachita kuti ndimvetsetse zonse za mapulaniwa."

20 Davide anatinso kwa mwana wake Solomoni, "Khala wamphamvu ndi
wolimba mtima ndipo uchite ntchitoyi. Usachite mantha kapena kutaya
mtima pakuti Yehova Mulungu wanga ali nawe. Iye sadzakukhumudwitsa
kapena kukusiya mpaka ntchito yonse ya Nyumba ya Mulungu itatha.
21 Magulu a ansembe ndi Alevi ndi okonzeka kugwira ntchito ya Nyumba
ya Mulungu, ndipo munthu waluso aliyense wodzipereka adzakuthandiza

pa ntchito yonse. Akuluakulu ndi anthu onse adzamvera chilichonse
chomwe udzalamula.”

# 29

*Zopereka Zomangira Nyumba ya Mulungu*

1 Kenaka, mfumu Davide inati kwa gulu lonse: “Mwana wanga
Solomoni amene Mulungu wamusankha ndi wamng’ono ndipo sadziwa
zambiri. Ntchitoyi ndi yayikulu chifukwa nyumba yaufumuyi si ya
munthu, koma ndi ya Yehova Mulungu. 2 Ine ndapereka ku ntchito
ya Nyumba ya Mulungu zinthu zanga zonse, golide wopangira zinthu
zagolide, siliva wopangira zinthu zasiliva ndi zitsulo zopangira zinthu
zazitsulo, mkuwa wopangira zinthu zamkuwa ndi matabwa opangira
zinthu zamatabwa komanso miyala yokongola ya onikisi yokongoletsera,
miyala ya maonekedwe osiyanasiyana, ndi miyala yonse yosalala ndi
miyala ya marabulo, zonsezi ndapereka zochuluka. 3 Kupatulapo izi,
ine modzipereka ku Nyumba ya Mulungu wanga, tsopano ndikupereka
chuma changachanga cha golide ndi siliva ku Nyumba ya Mulungu wanga,
kuwonjezera pa zimene ndapereka ku ntchito ya Nyumba ya Mulungu
woyerayu: 4 Matani 100 agolide (golide wa ku Ofiri) ndi matani 240 a
siliva woyengeka bwino wokutira makoma a nyumba, 5 zinthu zagolide ndi
zinthu zasiliva, ndiponso zinthu zonse zimene anthu aluso adzagwiritse
ntchito. Tsopano ndani amene akufuna kudzipatulira yekha kwa Yehova
lero?”

6 Tsono atsogoleri a mabanja, akuluakulu a mafuko a Israeli, olamulira
asilikali 1,000, ndi olamulira asilikali 100, ndiponso akuluakulu onse
amene amayang’anira ntchito ya mfumu anapereka mwaufulu. 7 Iwo
anapereka ku ntchito ya Nyumba ya Mulungu matani 170 a golide, matani
340 a siliva, matani 620 a mkuwa ndi matani 3,400 a chitsulo. 8 Aliyense
amene anali ndi miyala yokongola anayipereka ku nyumba yosungiramo
chuma cha Nyumba ya Yehova ndipo amene ankayang’anira anali Yehieli
Mgeresoni. 9 Anthu anakondwa chifukwa cha kupereka mwaufulu kwa
atsogoleri awo, pakuti anapereka kwa Yehova mwaufulu ndiponso ndi
mtima wonse. Nayenso mfumu Davide anakondwera kwambiri.

*Pemphero la Davide*

10 Davide anatamanda Yehova pamaso pa gulu lonse, ponena kuti,
“Mutamandidwe Inu Yehova
Mulungu wa kholo lathu Israeli
kuchokera muyaya mpaka muyaya.
11 Wanu, Inu Yehova ndi ukulu ndi mphamvu,
ulemerero ndiponso ufumu ndi kukongola.
Pakuti zinthu zonse zakumwamba ndi pa dziko lapansi ndi zanu.
Wanu, Inu Yehova ndi ufumu;
Inu ndinu wokwezeka ndipo ndinu mtsogoleri wa zonse.
12 Chuma ndi ulemu zimachokera kwa Inu;
Inu ndinu wolamulira zinthu zonse.
M’dzanja lanu muli nyonga ndi mphamvu,
kukweza ndi kupereka nyonga kwa onse.
13 Tsopano Mulungu wathu, ife tikukuthokozani
ndi kutamanda dzina lanu laulemerero.

14 “Koma ine ndine yani, ndipo anthu anga ndani, kuti tikupatsani
mowolowamanja motere? Zinthu zonse zimachokera kwa Inu, ndipo

ife takupatsani zomwe zimachokera m'dzanja lanu. 15 Ife ndife anthu
osadziwika ndiponso alendo pamaso panu, monga analili makolo athu.
Masiku anthu pa dziko lapansi ali ngati chithunzithunzi, wopanda chiyem-
bekezo. 16 Inu Yehova Mulungu wathu, zinthu zonse zimene tapereka
kumangira Nyumba yanu zachokera m'dzanja lanu ndipo zonsezi ndi
zanu. 17 Mulungu wanga, ine ndikudziwa kuti mumayesa mtima ndipo
mumakondwera ndi anthu angwiro. Zinthu zonsezi ndapereka mwaufulu
ndi cholinga chabwino. Ndipo tsopano ndaona ndi chimwemwe momwe
anthu anu amene ali pano akuperekera mwaufulu kwa Inu. 18 Inu Yehova
Mulungu wa makolo athu Abrahamu, Isake ndi Israeli, mukhazikitse
chofuna ichi m'mitima ya anthu anu kwamuyaya, ndipo mukhazikitse
mtima wokhulupirika kwa Inu. 19 Ndipo mumupatse mwana wanga
Solomoni mtima wodzipereka kwathunthu kwa Inu kuti asunge malamulo
anu, zofuna ndi malangizo anu. Achite chilichonse pomanga nyumba
yaufumu imene ine ndayipezera zofunika zonse."
20 Kenaka mfumu Davide inati kwa gulu lonse, "Tamandani Yehova
Mulungu wanu." Kotero onse anatamanda Yehova, Mulungu wa makolo
awo ndipo anawerama pansi ndi kugona chafufumimba pamaso pa
Yehova ndi mfumu.

### *Solomoni Avomerezedwa Monga Mfumu*

21 Mmawa mwake anthu anapereka nsembe zosiyanasiyana ndi nsembe
zopsereza kwa Yehova; ng'ombe zamphongo 1,000, nkhosa zamphongo
1,000 ndi ana ankhosa 1,000, pamodzi ndi nsembe yachakumwa ndi
nsembe zina zambiri zoperekera Aisraeli onse. 22 Tsiku limeneli, iwo
anadya ndi kumwa mosangalala pamaso pa Yehova ndipo anavomereza
Solomoni mwana wa Davide kukhala mfumu yawo kachiwiri.
Anamudzoza pamaso pa Yehova kukhala wolamulira wawo ndipo
Zadoki anadzozedwa kukhala wansembe. 23 Ndipo Solomoni ankakhala
pa mpando waufumu wa Yehova monga mfumu m'malo mwa Da-
vide abambo ake. Iye analemera ndipo Aisraeli onse ankamumvera.
24 Akuluakulu onse a ankhondo ndi anthu amphamvu, pamodzinso ndi
ana onse aamuna a mfumu Davide, analonjeza kumvera mfumu Solomoni.
25 Yehova anamukweza kwambiri Solomoni pamaso pa Aisraeli onse ndi
kumupatsa ulemerero waufumu umene sunapatsidwepo kwa mfumu ina
iliyonse ya Israeli.

### *Imfa ya Davide*

26 Davide mwana wa Yese anali mfumu ya Aisraeli onse. 27 Iye
analamulira Israeli kwa zaka makumi anayi; zaka zisanu ndi ziwiri ali ku
Hebroni ndi zaka 33 ali ku Yerusalemu. 28 Iye anamwalira atakalamba
kwambiri, atakhala ndi moyo wautali, chuma ndi ulemu. Solomoni
mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.
29 Tsono zonse zimene mfumu Davide anachita, kuyambira pachiyambi
mpaka pa mapeto, zalembedwa m'buku la mneneri Samueli, m'buku la
mneneri Natani ndi m'buku la mneneri Gadi, 30 pamodzi ndi tsatanetsa-
tane wa mbiri ya ulamuliro wake ndi mphamvu zake, ndi zonse zomwe
zinamuzungulira iye ndi Israeli ndiponso mafumu a mayiko ena onse.

# 2 Mbiri

*Solomoni Apempha Nzeru*

1 Solomoni mwana wa Davide anakhazikika molimbika mu ufumu wake,
pakuti Yehova Mulungu wake anali naye ndipo anamukweza kwambiri.

2 Tsono Solomoni anayankhula kwa Aisraeli onse, olamulira a anthu
1,000, olamulira a anthu 100, oweruza ndiponso kwa atsogoleri onse a
Israeli ndi atsogoleri amabanja. 3 Solomoni pamodzi ndi gulu lonse la
anthu anapita ku malo ofunika kwambiri pachipembedzo ku Gibiyoni.
Tenti ya msonkhano ya Mulungu inali kumeneko, imene Mose mtumiki
wa Yehova anayipanga m'chipululu muja. 4 Davide anabweretsa Bokosi la
Mulungu kuchokera ku Kiriyati Yearimu, ndi kulikhazika kumalo kumene
analikonzera popeza analimangira tenti mu Yerusalemu. 5 Koma guwa
lansembe lamkuwa limene Bezaleli mwana wa Uri, mwana wa Huri
analipanga linali ku Gibiyoni kutsogolo kwa tenti ya Yehova. Kotero kuti
Solomoni ndi gulu lonse anakapembedza kumeneko. 6 Solomoni anapita
pamene panali guwa lansembe lamkuwa pamaso pa Yehova mu tenti ya
msonkhano ndipo anapereka nsembe zopsereza 1,000.

7 Usiku umenewo Mulungu anaonekera kwa Solomoni ndipo anati kwa
iye, "Pempha chilichonse chimene ukufuna ndipo ndidzakupatsa."

8 Solomoni anayankha Mulungu kuti, "Inu munaonetsa kukoma mtima
kwakukulu kwa Davide abambo anga ndipo mwayika ine kukhala mfumu
m'malo mwake. 9 Tsopano Inu Yehova Mulungu, lolani kuti lonjezo lanu
kwa abambo anga Davide likwaniritsidwe, pakuti mwandiyika kukhala
mfumu ya anthu anu amene ndi ochuluka ngati fumbi la pa dziko lapansi.
10 Mundipatse nzeru ndi luntha zolamulira anthu awa, pakuti ndani
amene angathe kulamulira anthu anu ochulukawa?"

11 Mulungu anati kwa Solomoni, "Popeza izi ndi zokhumba za mtima
wako ndipo sunapemphe katundu, chuma kapena ulemu, kapena imfa
ya adani ako, ndiponso poti sunapemphe moyo wautali koma nzeru
ndi luntha kuti ulamulire anthu anga amene Ine ndakuyika kukhala
mfumu yawo, 12 Ine ndidzakupatsa nzeru ndi chidziwitso. Ndipo
ndidzakupatsanso katundu, chuma ndi ulemu, zinthu zoti palibe mfumu
imene inali nazo iwe usanakhalepo ndipo palibe wina amene adzakhale
nazo iweyo ukadzafa."

13 Kotero Solomoni anabwerera ku Yerusalemu kuchoka kumalo opem-
bedzerako a ku Gibiyoni, ku tenti ya msonkhano ndipo analamulira Israeli.

14 Solomoni anasonkhanitsa magaleta ndi akavalo; anali ndi magaleta
1,400 ndi akavalo 12,000, amene anawayika m'mizinda yosungira maga-
leta ndipo ena anali ndi iye mu Yerusalemu. 15 Mfumu inasandutsa siliva
ndi golide kukhala ngati miyala wamba mu Yerusalemu. Inasandutsanso
mkungudza kukhala wochuluka ngati mitengo ya mkuyu ya ku zigwa.
16 Solomoni amagula akavalo ku Igupto ndi Kuwe pakuti anthu amalonda
a mfumu amakawagula ku Kuwe. 17 Anthu ankagula galeta ku Igupto
pa mtengo wa masekeli asiliva 600 ndipo kavalo pa mtengo wa ndalama
zasiliva 150. Iwo ankazigulitsanso kwa mafumu onse a Ahiti ndi a Aramu.

# 2

### *Kukonzekera Kumanga Nyumba ya Mulungu*

1 Solomoni anatsimikiza zoti amange Nyumba ya Dzina la Yehova ndi
nyumba yake yaufumu. 2 Iye analemba ntchito anthu 70,000 onyamula
katundu ndi anthu 80,000 okumba miyala ku mapiri ndiponso akapitawo
3,600 oyang'anira anthuwo.

3 Solomoni anatumiza uthenga uwu kwa Hiramu mfumu ya ku Turo:
"Munditumizire mitengo ya mkungudza monga munachitira ndi
abambo anga pamene munawatumizira mitengo ya mkungudza yomangira
nyumba yaufumu yokhalamo. 4 Tsono ine ndikufuna kumanga
Nyumba ya Yehova Mulungu wanga ndi kuyipereka kwa Iye kuti
tiziyikamo buledi wopatulika nthawi zonse ndiponso kuperekeramo
nsembe zopsereza mmawa uliwonse ndi madzulo ndi pa masabata ndi
pa masiku a chikondwerero cha mwezi watsopano ndiponso pa masiku
osankhika a chikondwerero cha Yehova Mulungu wathu, monga mwa
malamulo a Aisraeli mpaka muyaya.

5 "Nyumba ya Mulungu imene ndidzamange idzakhala yayikulu,
chifukwa Mulungu wathu ndi wamkulu kuposa milungu ina yonse.
6 Koma ndani angathe kumumangira Iye Nyumba, pakuti mlengalenga,
ngakhale kumwamba kwenikweni sikungamukwane? Tsono ine ndine
yani kuti ndimangire Iyeyo Nyumba, kupatula malo chabe opserezerapo
nsembe pamaso pake?

7 "Tsono tumizireni munthu waluso pa ntchito zagolide ndi siliva,
mkuwa ndi chitsulo, nsalu yapepo ndi yofiira ndi yobiriwira ndiponso
waluso losema, kuti adzagwire ntchito mu Yuda ndi Yerusalemu
pamodzi ndi anthu aluso amene abambo anga Davide anandipatsa.

8 "Munditumizirenso mitengo ya mkungudza, payini ndiponso
matabwa a m'bawa wa ku Lebanoni, pakuti ndikudziwa kuti anthu
anu ali ndi luso locheka matabwa kumeneko. Antchito anga adzagwira
ntchito pamodzi ndi antchito anu 9 kuti andipatse matabwa ambiri,
chifukwa Nyumba imene ndikumanga iyenera kukhala yayikulu ndi
yokongola. 10 Ine ndidzalipira antchito anu amene adzacheke matabwa
matani 1,000 a tirigu wopunthapuntha, matani 2,000 a barele, malita
440,000 a vinyo, ndiponso malita 440,000 a mafuta a olivi."

11 Hiramu, mfumu ya ku Turo, anamuyankha Solomoni pomulembera
kalata kuti,
"Chifukwa Yehova amakonda anthu ake, wayika iwe kukhala mfumu
yawo."

12 Ndipo Hiramu anawonjezera kunena kuti,
"Atamandike Yehova Mulungu wa Israeli, amene analenga
kumwamba ndi dziko lapansi! Iye wamupatsa Davide mwana wanzeru,
wodzaza ndi luntha ndi wozindikira, amene adzamanga Nyumba ya
Mulungu ndi kudzimangira yekha nyumba yaufumu.

13 "Ine ndikukutumizira Hiramu Abi, munthu wa luso lalikulu,
14 amene amayi ake anali wochokera ku Dani ndipo abambo ake anali
a ku Turo. Iye anaphunzitsidwa kugwira ntchito zagolide ndi siliva,
mkuwa ndi chitsulo, miyala yokongola ndi matabwa, ndiponso nsalu
zofewa zobiriwira, zapepo ndi zofiira. Alinso ndi luso la zosemasema
ndipo atha kupanga chilichonse chimene wapatsidwa. Iye adzagwira
ntchito ndi amisiri anu ndi a mbuye wanga, Davide abambo anu.

[15] "Tsono mbuye wanga tumizirani antchito anu tirigu ndi barele,
mafuta a olivi ndi vinyo zimene mwalonjeza, [16] ndipo ife tidzadula
mitengo yonse imene mukuyifuna kuchokera ku Lebanoni ndipo tidza-
yimanga pamodzi ndi kuyiyadamitsa pa madzi mpaka ku Yopa. Ndipo
inu mudzatha kuyitenga mpaka ku Yerusalemu."

[17] Solomoni anawerenga alendo onse amene anali mu Israeli, potsatira
chiwerengero chimene abambo ake Davide anachita ndipo panapezeka
kuti analipo anthu 153,600. [18] Iye anayika anthu 70,000 kuti akhale
onyamula katundu ndi anthu 80,000 kuti akhale ophwanya miyala
m'mapiri, anthu 3,600 anawayika kukhala akapitawo oyang'anira anthu
pa ntchitoyo.

# 3

## *Solomoni Amanga Nyumba ya Mulungu*

[1] Pamenepo Solomoni anayamba kumanga Nyumba ya Yehova mu
Yerusalemu pa Phiri la Moriya, pamene Yehova anaonekera Davide
abambo ake. Panali pabwalo lopunthirapo tirigu la Arauna Myebusi, malo
amene anapereka Davide. [2] Iye anayamba kumanga pa tsiku lachiwiri la
mwezi wachiwiri m'chaka chachinayi cha ulamuliro wake.

[3] Maziko amene Solomoni anayika pomanga Nyumba ya Mulungu ndi
awa: Mulitali munali mamita 27, mulifupi munali mamita asanu ndi anayi
(potsata miyeso yakale). [4] Chipinda cha polowera mulitali mwake chinali
mamita asanu ndi anayi ofanana ndi mulifupi mwake mwa nyumbayo.
Msinkhu wake unali mamita 54.

Iye anakuta nyumbayo m'kati mwake ndi golide woyengeka bwino.
[5] Chipinda chachikulu, khoma lake anakhomera matabwa a payini
ndipo analikutira ndi golide wabwino ndi kulikongoletsa ndi zithunzi za
kanjedza ndi maunyolo. [6] Iye anakongoletsa Nyumba ya Mulunguyo ndi
miyala yokongola. Ndipo golide amene anagwiritsa ntchito anali golide wa
ku Paravaimu. [7] Iye anakutira ndi golide mitanda ya ku denga, maferemu
a zitseko, makoma ndi zitseko za Nyumba ya Mulungu, ndipo anajambula
Akerubi m'makoma mwake.

[8] Iye anamanga Malo Opatulika Kwambiri ndipo mulitali mwake munali
mofanana ndi mulifupi mwa Nyumba mamita asanu ndi anayi. Anakuta
m'kati mwake ndi golide wosalala wolemera matani makumi awiri.
[9] Misomali yagolide imalemera magalamu 570. Anakutanso ndi golide
zipinda zapamwamba.

[10] Ku Malo Opatulika Kwambiri iye anapangako Akerubi awiri achitsulo
ndipo anawakuta ndi golide. [11] Kutalika kwa mapiko onse a Akerubi kunali
mamita asanu ndi anayi. Phiko la Kerubi woyamba linali loposerapo
mamita awiri ndipo limakhudza khoma la Nyumba ya Mulungu, pamene
phiko linalo, lotalikanso koposerapo mamita awiri, limakhudza phiko
la Kerubi winayo. [12] Chimodzimodzinso phiko la Kerubi wachiwiri
linali loposerapo mamita awiri ndipo limakhudza mbali ina ya khoma
la Nyumba ya Mulungu, ndipo linalo limene linalinso loposera mamita
awiri, limakhudza phiko la Kerubi woyamba uja. [13] Mapiko a Akerubiwa
akawatambasula amatalika mamita asanu ndi anayi. Akerubiwa anay-
imirira pa mapazi awo, kuyang'ana chipinda chachikulu.

[14] Solomoni anapanga nsalu zotchingira zobiriwira, zapepo ndi zofiira
ndi nsalu zofewa zosalala, atajambulapo Akerubi.

[15] Kutsogolo kwa Nyumba ya Mulungu anamangako zipilala ziwiri,
zimene zonse pamodzi zinali zotalika mamita khumi ndi asanu ndi theka;
chipilala chilichonse chinali ndi mutu woposera mamita awiri. [16] Iye ana-
panga maunyolo olumikizanalumikizana ndipo anawayika pamwamba
pa zipilalazo. Anapanganso makangadza 100 ndipo anawalumikiza
ku maunyolo aja. [17] Solomoni anayimika nsanamirazo kutsogolo kwa
Nyumba ya Mulungu, imodzi mbali ya kummwera ndi inayo mbali ya
kumpoto. Nsanamira ya kummwera anayitcha Yakini ndipo ya kumpoto
anayitcha Bowazi.

# 4

*Zipangizo za m'Nyumba ya Mulungu*

[1] Solomoni anapanga guwa lamkuwa limene mulitali mwake linali
mamita asanu ndi anayi, mulifupi mwakenso mamita asanu ndi anayi
ndipo msinkhu wake unali mamita anayi ndi theka. [2] Kenaka iye anapanga
mbiya yayikulu yachitsulo. Inali yozungulira ndipo pakamwa pake panali
pa mamita anayi ndi theka, poyeza modutsa pakati pake. Msinkhu
wake unali wopitirirapo mamita awiri. Thunthu lake linali mamita
13. [3] M'munsi mwa mkombero wa mbiyayo anajambulamo zithunzi
zang'ombe zazimuna mozungulira, zithunzi khumi pa theka la mita.
Ng'ombezo zimajambulidwa m'mizere iwiri ndipo anazipangira kumodzi
ndi mbiyayo.

[4] Mbiyayo anayisanjika pa ng'ombe zamkuwa khumi ndi ziwiri, zitatu
zoyang'ana kumpoto, zitatu zoyang'ana kumadzulo, zitatu zoyang'ana
kummwera ndipo zitatu zoyang'ana kummawa. Mbiyayo inakhazikika
pamwamba pa ng'ombezo, ndipo miyendo yake yonse yakumbuyo ya
ng'ombezo inkaloza m'kati. [5] Mbiyayo inali yochindikala ngati chikhatho
ndipo mkombero wake unali ngati mkombero wa chikho, ngati duwa
lokongola kwambiri. M'mbiyamo munkalowa madzi okwana malita
60,000.

[6] Kenaka anapanga mabeseni khumi otsukira zinthu ndipo asanu am-
awayika mbali ya kummwera, asanu mbali ya kumpoto. M'menemo am-
atsukiramo zinthu zimene zimagwiritsidwa ntchito pa nsembe zopsereza
koma mbiyamo ndi m'mene ankasambiramo ansembe.

[7] Solomoni anapanga zoyikapo nyale khumi zagolide monga momwe
kunalembedwera ndipo anaziyika m'Nyumba ya Mulungu, zisanu mbali
ya kummwera, ndi zisanu mbali ya kumpoto.

[8] Iye anapanga matebulo khumi ndipo anawayika m'Nyumba ya
Mulungu, asanu mbali ya kummwera ndi asanu mbali ya kumpoto. Iye
anapanganso mabeseni agolide okwanira 100.

[9] Iye anapanga bwalo la ansembe, bwalo lalikulu ndi zitseko za
bwalolo ndipo anakuta zitsekozo ndi mkuwa. [10] Anayika mbiya ija mbali
yakummwera pamene mbali ya kummawa ndi kummwera zimakumana.

[11] Iye anapanganso miphika ndi mafosholo ndi mabeseni owazira
magazi.

Kotero Hiramu anatsiriza ntchito yonse ya ku Nyumba ya Mulungu
imene ankagwirira Mfumu Solomoni:

[12] Nsanamira ziwiri;
mbale ziwiri za mitu yapamwamba pa nsanamirazo;
maukonde awiri okongoletsera mbale ziwiri za mitu yapamwamba pa
nsanamirazo;

13 makangadza 400 a maukonde awiri okongoletserawo (mizere iwiri ya makangadza pa ukonde uliwonse, kukongoletsa mbale za mitu yapamwamba pa nsanamira);
14 miyendo pamodzi ndi mabeseni ake;
15 mbiya pamodzi ndi ng'ombe khumi ndi ziwiri zazimuna zosanjikapo mbiyayo.
16 Miphika, mafosholo, mafoloko otengera nyama ndi ziwiya zina zonse.

Zipangizo zonse zimene Hiramu Abi anapangira Mfumu Solomoni
za m'Nyumba ya Yehova zinali zamkuwa wonyezimira. 17 Mfumu
inapangitsa zimenezi m'chigwa cha Yorodani, ku malo amtapo amene
anali pakati pa Sukoti ndi Zaretani. 18 Zinthu zonse zimene Solomoni
anapanga zinali zochuluka kwambiri kotero kuti kulemera kwa mkuwa
sikunadziwike.
19 Solomoni anapanganso ziwiya zonse zimene zinali m'Nyumba ya
Mulungu:

guwa lansembe lagolide;
matebulo pamene ankayikapo buledi woperekedwa kwa Mulungu;
20 zoyikapo nyale zagolide ndi nyale zake zagolide weniweni, kuti ziziyaka m'kati mwenimweni mwa malo opatulika monga analembera,
21 maluwa agolide, nyale ndi mbaniro. (Zinali zagolide mmodzi);
22 zozimitsira nyale zagolide weniweni, mbale zowazira magazi, mbale ndi zofukizira; ndiponso zitseko zagolide za Nyumba ya Mulungu, chitseko cha ku Malo Opatulika Kwambiri ndi zitseko za ku chipinda chachikulu.

# 5

1 Pamene ntchito yonse imene Solomoni anagwira pa Nyumba ya
Yehova inatha, anabwera ndi zinthu zonse zimene abambo ake Davide
anazipereka; siliva, golide ndi ziwiya. Anaziyika m'zipinda zosungiramo
chuma cha ku Nyumba ya Mulungu.

*Bokosi la Chipangano Libweretsedwa m'Nyumba ya Mulungu*

2 Kenaka Solomoni anasonkhanitsa akuluakulu a Israeli mu Yerusalemu,
atsogoleri onse a mafuko ndi akuluakulu a mabanja a Aisraeli, kuti
akatenge Bokosi la Chipangano la Yehova ku Ziyoni, mzinda wa Da-
vide. 3 Ndipo Aisraeli onse anasonkhana pamaso pa mfumu nthawi ya
chikondwerero cha mwezi wachisanu ndi chiwiri.
4 Akuluakulu onse a Israeli atafika, Alevi ananyamula Bokosi la
Chipangano, 5 ndipo anabwera nalo bokosi lija pamodzi ndi tenti
ya msonkhano ndi ziwiya zonse zopatulika zimene zinali m'menemo.
Ansembe ndi Alevi ndiye anazinyamula, 6 ndipo Mfumu Solomoni ndi
gulu lonse la Aisraeli amene anasonkhana naye anali patsogolo pa Bokosi
la Chipangano, akupereka nsembe nkhosa zambiri ndi ng'ombe zambiri
zosawerengeka.
7 Ansembe anafika nalo Bokosi la Chipangano la Yehova m'chipinda
cham'kati mwenimweni, Malo Opatulika Kwambiri, ndipo analiyika pansi
pa mapiko a Akerubi. 8 Akerubiwo anatambalitsa mapiko awo pamwamba
pa Bokosi la Chipangano ndipo anaphimba bokosilo pamodzi ndi mitengo
yonyamulira. 9 Mitengoyi inali yayitali kwambiri ndipo inkaonekera kunja

kwa chipinda cham'kati cha Malo Opatulika, koma osati kunja kwa Malo
Opatulikawo; ndipo mitengoyi ilipo mpaka lero lino. 10 M'bokosimo
munalibe kanthu kena kalikonse kupatula miyala iwiri imene Mose
anayikamo ku Horebu, kumene Yehova anachita pangano ndi Aisraeli
atatuluka m'dziko la Igupto.

11 Kenaka ansembe anatulukamo m'Malo Opatulika. Ansembe onse
amene anali m'menemo anali atadziyeretsa posayang'aniranso magulu
awo ochokera. 12 Alevi onse amene anali oyimba: Asafu, Hemani, Yedutuni
ndi ana ndiponso abale awo, amayima mbali ya kummawa kwa guwa
lansembe atavala zovala zofewa zosalala akuyimba ziwaya zamalipenga,
azeze ndi apangwe. Ansembe onse amene amayimba malipenga analipo
120 pamodzi. 13 Oyimba malipenga ndi oyimba nyimbo aja amayimba
mogwirizana, monga liwu la munthu mmodzi, kutamanda ndi kuyamika
Yehova. Mogwirizana ndi malipenga, ziwaya zamalipenga ndi zida zina,
anakweza mawu awo motamanda Yehova poyimba kuti,

"Yehova ndi wabwino;
chikondi chake chikhala mpaka muyaya."

Ndipo Nyumba ya Mulungu wa Yehova inadzaza ndi mtambo, 14 choncho
ansembe sanathe kugwira ntchito yawo chifukwa cha mtambowo, pakuti
ulemerero wa Yehova unadzaza Nyumba ya Mulungu.

# 6

1 Pamenepo Solomoni anati, "Yehova anati adzakhala m'mitambo
yakuda; 2 ine ndakumangirani Nyumba yokongola kwambiri, malo woti
muzikhalamo mpaka muyaya."

3 Aisraeli onse ali chiyimire pomwepo, mfumu inatembenuka ndi
kuwadalitsa. 4 Ndipo inati,

"Atamandike Yehova, Mulungu wa Israeli amene wachita ndi dzanja
lake zimene analonjeza ndi pakamwa pake kwa Davide abambo anga.
Pakuti Iye anati, 5 'Kuyambira tsiku limene ndinatulutsa anthu anga
ku Igupto, sindinasankhe mzinda wina uliwonse pa fuko lina lililonse
la Aisraeli kuti kumeneko andimangire Nyumba kuti ndizikhalamo
kapena munthu wina aliyense kuti akhale mtsogoleri wa Aisraeli anthu
anga. 6 Koma tsopano ndasankha Yerusalemu kuti Dzina langa likhale
kumeneko ndiponso ndasankha Davide kuti alamulire anthu anga
Aisraeli.'

7 "Abambo anga Davide anali ndi maganizo mu mtima mwawo
oti amangire Nyumba Yehova Mulungu wa Israeli. 8 Koma Yehova
ananena kwa abambo anga Davide kuti, 'Popeza zinali mu mtima
mwako kumangira Nyumba dzina langa, unachita bwino kukhala ndi
maganizo amenewa mu mtima mwakomo. 9 Komatu si iwe amene
udzamanga Nyumba ya Mulungu koma mwana wako, mwana amene
iwe udzabereke. Iyeyo ndiye amene adzandimangire Nyumba.'

10 "Yehova wasunga zimene analonjeza. Ine ndalowa m'malo mwa
abambo anga Davide, ndipo tsopano ndili pa mpando waufumu wa
Israeli, monga momwe Yehova analonjezera, ndipo ndamangira nyumba
Dzina la Yehova Mulungu wa Israeli. 11 M'menemo ndayikamo Bokosi
la Chipangano, mmene muli pangano la Yehova limene anapangana ndi
ana a Israeli."

*Pemphero la Solomoni*

12 Pamenepo Solomoni anayimirira patsogolo pa guwa lansembe la
Yehova patsogolo pa gulu lonse la Aisraeli ndipo anakweza manja ake.
13 Iyeyo anali atapanga nsanja yamkuwa, kutalika kwake kunali mamita
awiri, mulifupi mwake munali mamita awiri, msinkhu wake unali mita
imodzi ndi theka ndipo nsanjayo anayimika pakati pa bwalo lakunja. Iye
anayimirira pa nsanjapo nagwada pamaso pa gulu lonse la Aisraeli ndipo
anakweza manja ake kumwamba. 14 Iye anati,

"Inu Yehova, Mulungu wa Israeli, palibe Mulungu wofanana nanu
kumwamba kapena pa dziko. Inu amene mumasunga pangano ndi
kuonetsa chikondi chosasinthika kwa atumiki anu amene amayenda
pamaso panu ndi mtima wawo wonse. 15 Inu mwasunga lonjezo lanu
kwa abambo anga Davide, mtumiki wanu. Inde zimene munalonjeza
ndi pakamwa panu, mwazikwaniritsa ndi manja anu monga mmene
tikuonera lero lino.

16 "Ndipo tsopano, Inu Yehova Mulungu wa Israeli, sungani zimene
munalonjeza kwa abambo anga Davide, mtumiki wanu pamene munati,
'Sudzasowa munthu wokhala pamaso panga pa mpando waufumu wa
Israeli, ngati ana ako adzasamalira mayendedwe awo ndi kusunga
malamulo anga monga iwe wachitira.' 17 Ndipo tsopano Inu Yehova,
Mulungu wa Israeli, lolani kuti mawu anu akwaniritsidwe amene
munalonjeza mtumiki wanu Davide.

18 "Kodi Mulungu angakhaledi pa dziko lapansi ndi munthu? Mlen-
galenga ngakhale kumwamba kwenikweni sikungakukwaneni. Nanga
kuli bwanji ndi Nyumba iyi imene ndamanga! 19 Koma Inu Yehova,
Mulungu wanga, imvani pemphero ndi pembedzero la mtumiki wanu.
Imvani kulira ndi pemphero la mtumiki wanu limene ndikupempha
pamaso panu. 20 Maso anu azikhala otsekuka kuyang'ana Nyumba ino
usana ndi usiku, malo ano amene Inu munati mudzayikamo Dzina lanu,
imvani pemphero la mtumiki wanu limene akupemphera pa malo ano.
21 Imvani mapembedzero a mtumiki wanu ndi a anthu anu Aisraeli
pamene akupemphera akuyang'ana malo ano. Imvani kumwambako,
malo anu amene mumakhala; ndipo mukamva muzitikhululukira.

22 "Munthu akalakwira mnzake, nawuzidwa kuti alumbire, akabwera
kudzalumbira patsogolo pa guwa lansembe la Nyumba ino, 23 imvani
kumwambako ndi kuchitapo kanthu. Weruzani atumiki anuwo,
wochimwa mugamule kuti ndi wolakwa ndipo alangidwe chifukwa
cha zimene wachita. Wosachimwa mugamule kuti wosalakwa, ndipo
muonetse kusalakwa kwakeko.

24 "Anthu anu Aisraeli akagonja kwa adani awo chifukwa
akuchimwirani ndipo akatembenukira kwa Inu ndi kuvomereza Dzina
lanu, kupemphera ndi kupembedzera pamaso panu m'Nyumba ino,
25 pamenepo imvani kumwambako ndi kukhululukira tchimo la anthu
anu Aisraeli ndi kuwabweretsa ku dziko limene munawapatsa iwo ndi
makolo awo.

26 "Pamene kumwamba kwatsekeka ndipo mvula sikugwa chifukwa
anthu anu akuchimwirani, ndipo pamene apemphera akuyang'ana
malo ano ndi kuvomereza Dzina lanu ndi kutembenuka kuchoka
ku machimo awo chifukwa inu mwawalanga, 27 pamenepo imvani
kumwambako ndipo muwakhululukire atumiki anu, anthu anu Aisraeli.
Aphunzitseni makhalidwe oyenera, ndipo gwetsani mvula m'dziko
limene munapereka kwa anthu anu monga cholowa chawo.

28 "Pamene m'dziko mwagwa njala kapena mliri, chinoni kapena
chiwawu, dzombe kapena kapuchi, kapena pamene adani azungulira

mzinda wawo wina uliwonse, kaya mavuto kapena matenda abwera,
29 ndipo wina aliyense mwa Aisraeli akapemphera kapena kukudan-
daulirani, aliyense wa iwo akadziwa masautso ake ndi ululu wake,
ndi kukweza manja awo kuloza Nyumba ino, 30 pamenepo imvani
kumwambako, malo anu wokhalamo. Khululukani ndipo muchitire aliyense molingana ndi zonse zimene anachita popeza Inu mumadziwa mtima wake, (pakuti ndinu nokha amene mumadziwa mitima ya anthu),
31 motero iwo adzakuopani ndipo adzayenda m'njira zanu masiku onse amene adzakhale m'dziko limene munalipereka kwa makolo athu.

32 "Ndipo kunena za mlendo amene si mmodzi wa anthu anu Aisraeli, koma wabwera kuchokera ku dziko lakutali chifukwa cha dzina lanu lotchukali, ndiponso za dzanja lanu lamphamvu ndi lochita
zazikulu, kudzapemphera akuyang'ana Nyumba ino, 33 pamenepo
imvani kumwambako, malo anu okhalamo, ndipo muchite zonse zimene mlendoyo akukupemphani, kotero kuti anthu onse a dziko lapansi adziwe dzina lanu ndi kukuopani monga amachitira anthu anu Aisraeli, ndipo adziwe kuti nyumba ino imene ndakumangirani imadziwika ndi dzina lanu.

34 "Anthu akapita ku nkhondo kukamenyana ndi adani awo, kulikonse kumene mungawatume, ndipo akapemphera moyang'ana mzinda uno umene mwausankha ndi Nyumba yanu imene ndakumangirani,
35 pamenepo imvani kumwamba pemphero lawo ndi kupempha kwawo ndipo muwapulumutse.

36 "Pamene achimwira inu, pakuti palibe amene sachimwa, ndipo inu mwawakwiyira ndi kuwapereka kwa adani awo, amene awatenga
ukapolo ku dziko lawo lakutali kapena pafupi. 37 Ngati asintha mitima
yawo ku dziko limene ali akapolo ndi kulapa ndi kukudandaulirani inu m'dziko la ukapolo wawo ndi kunena kuti, 'Ife tachimwa, tachita
zolakwa ndipo tachita moyipa kwambiri.' 38 Ndipo ngati atembenukira
kwa inu ndi mtima ndi moyo wawo wonse m'dziko lawo la ukapolo kumene anatengedwako ndi kupemphera moyang'ana dziko limene inu munalipereka kwa makolo awo, moyang'ana Nyumba yanu imene
ndakumangirani; 39 pamenepo imvani kumwamba, malo anu okhala,
pemphero lawo ndi kudandaula kwawo, ndipo muwapulumutse. Ndipo mukhululukire anthu anu, amene akuchimwirani.

40 "Tsono Inu Mulungu wanga, tsekulani maso anu ndi makutu anu kuti mumve mapemphero ochitikira pa malo ano.

41 "Tsopano dzukani Inu Yehova Mulungu, ndipo bwerani ku malo anu ampumulo,
Inu ndi Bokosi la Chipangano la mphamvu zanu.
Inu Yehova Mulungu, ansembe anu avale chipulumutso,
oyera mtima anu akondwere ndi kukhulupirika kwanu.
42 Inu Yehova Mulungu musamukane wodzozedwa wanu.
Kumbukirani chikondi chanu chachikulu chimene munalonjeza kwa Davide mtumiki wanu."

# 7

*Mwambo Wopereka Nyumba kwa Yehova*

1 Solomoni atamaliza kupemphera, moto unatsika kuchokera kumwamba ndi kutentha nsembe zopsereza ndi nsembe zina, ndipo
ulemerero wa Yehova unadzaza Nyumba ya Mulunguyo. 2 Ansembe
sanathe kulowa m'Nyumba ya Mulungu chifukwa munadzaza ulemerero

wa Yehova. [3] Aisraeli onse ataona moto ukuchokera kumwamba ndi
ulemerero wa Yehova pamwamba pa Nyumba ya Mulungu, anagwada
poyalidwa miyalapo ndipo anagunditsa nkhope zawo pansi, ndi kulambira
ndi kutamanda Yehova, ponena kuti,

"Iye ndi wabwino;
chikondi chake chikhala chikhalire"

[4] Tsono mfumu ndi anthu onse anapereka nsembe pamaso pa Yehova.
[5] Ndipo mfumu Solomoni anapereka nsembe ng'ombe 22,000, nkhosa
ndi mbuzi 120,000. Kotero mfumu ndi anthu onse anachita mwambo
wopereka Nyumba kwa Mulungu. [6] Ansembe anayimirira m'malo
mwawo, monganso anachitira Alevi ndi zida zoyimbira za Yehova, zimene
Davide anapanga zotamandira Yehova ndipo zimagwiritsidwa ntchito
pamene amatamanda, ponena kuti, "Chikondi chake chikhale chikhalire."
Moyang'anizana ndi Alevi, ansembe amaliza malipenga, ndipo Aisraeli
onse anali atayimirira.

[7] Solomoni anapatula malo a pakati pa bwalo kutsogolo kwa Nyumba
ya Yehova ndipo pamenepo anapereka nsembe zopsereza ndi mafuta,
zopereka za chiyanjano, chifukwa guwa lansembe lamkuwa limene
anapanga panalibe malo woti n'kuperekerapo nsembe zopsereza, nsembe
za ufa ndi mafuta.

[8] Choncho nthawi imeneyi, Solomoni anachita chikondwerero kwa
masiku asanu ndi awiri pamodzi ndi Aisraeli onse. Unali msonkhano
waukulu, kuyambira ku Lebo Hamati mpaka ku chigwa cha ku Igupto. [9] Pa
tsiku lachisanu ndi chitatu panali msonkhano, pakuti anachita mwambo
wopereka guwa lansembe kwa masiku asanu ndi awiri ndi masiku enanso
asanu ndi awiri achikondwerero. [10] Pa tsiku la 23 la mwezi wachisanu
ndi chiwiri, Solomoni anawuza anthu aja kuti apite kwawo. Anthu
anali achimwemwe ndi okondwa m'mitima mwawo chifukwa cha zinthu
zabwino zimene Yehova anachitira Davide ndi Solomoni ndiponso anthu
ake Aisraeli.

### *Yehova Aonekera Solomoni*

[11] Solomoni atatsiriza kumanga Nyumba ya Yehova ndi nyumba yau-
fumu ndi kukwaniritsa kuchita zonse zimene zinali mu mtima mwake pa
Nyumba ya Yehova ndi nyumba yake yaufumu, [12] Yehova anamuonekera
usiku ndipo anati:

"Ine ndamva pemphero lako ndipo ndadzisankhira malo ano kukhala
Nyumba yanga yoperekeramo nsembe.

[13] "Ine ndikatseka kumwamba kuti mvula isagwe, kapena kulamulira
dzombe kuti liwononge dziko, kapena kutumiza mliri pakati pa anthu,
[14] ngati anthu anga, amene amatchedwa ndi dzina langa adzichepetsa
ndi kupemphera ndi kufunafuna nkhope yanga, nasiya njira zawo
zoyipa, pamenepo Ine ndidzamva kumwamba ndipo ndidzakhululuka
tchimo lawo ndi kuchiritsa dziko lawo. [15] Ndipo maso anga adzatsekuka
ndi makutu anga adzakhala tcheru kumva mapemphero a pamalo
pano. [16] Ine ndasankha ndipo ndapatula Nyumba yangayi kotero
kuti ndidzakhala m'menemo kwamuyaya. Maso ndi mtima wanga
zidzakhala pano nthawi zonse.

[17] "Kunena za iwe, ukayenda pamaso panga mokhulupirika monga
momwe anachitira abambo ako Davide, ndi kuchita zonse zimene
ndakulamula, ndi kusamalitsa malangizo ndi malamulo anga, [18] Ine
ndidzakhazikitsa mpando wako waufumu, monga ndinachitira pangano

ndi abambo ako Davide pamene ndinati, 'Sipadzasowa munthu wola-
mulira Israeli.'
[19] "Koma ngati iwe udzapatuka ndi kutaya malangizo ndi malamulo
amene ndakupatsa ndi kupita kukatumikira milungu ina ndi kuyipem-
bedza, [20] pamenepo Ine ndidzazula Aisraeli m'dziko langa limene ndi-
nawapatsa, ndiponso ndidzayikana Nyumba ino imene ndadzipatulira.
Ndipo udzakhala ngati mwambi ndi chinthu chonyozedwa pakati pa
anthu onse. [21] Ndipo ngakhale kuti tsopano Nyumba ya Mulunguyi ndi
yokongola kwambiri, onse amene adzadutsa pano adzadabwa kwambiri
ndipo adzati, 'N'chifukwa chiyani Yehova wachita chinthu chotere
m'dziko muno ndi pa Nyumba ya Mulunguyi?' [22] Anthu adzayankha
kuti, 'N'chifukwa chakuti asiya Yehova, Mulungu wa makolo awo,
amene anawatulutsa m'dziko la Igupto ndipo akangamira milungu
ina ndi kumayipembedza ndi kuyitumikira. Choncho Iye wabweretsa
zovuta zonsezi.' "

# 8

*Ntchito Zina za Solomoni*

[1] Patatha zaka makumi awiri, ndiye nthawi imene Solomoni anamanga
Nyumba ya Mulungu ndi nyumba yake yaufumu, [2] Solomoni anamanganso
midzi imene anapatsidwa ndi Hiramu, ndipo anakhazikamo Aisraeli.
[3] Kenaka Solomoni anapita kukalanda Hamati-zoba. [4] Iye anamanganso
Tadimori ku chipululu ndi mizinda yonse yosungiramo chuma, imene
anayimanga ku Hamati. [5] Anamanganso Beti-Horoni Wakumtunda ndi
Beti-Horoni Wakumunsi, mizinda yotetezedwa yokhala ndi makoma,
zitseko ndi zitsulo zotchingira, [6] pamodzinso ndi Baalati ndi mizinda yake
yonse yosungira chuma, ndiponso mizinda yonse yosungiramo magaleta
ake ndi akavalo ndi chilichonse anafuna kumanga ku Yerusalemu, ku
Lebanoni ndi ku madera onse amene iye ankalamulira.

[7] Panali anthu amene anatsala pakati pa mitundu ya Ahiti, Aamori,
Aperezi, Ahivi ndi Ayebusi (anthu awa sanali Aisraeli). [8] Zimenezi ndiye
zinali zidzukulu zawo zotsalira m'dzikoli, anthu amene Aisraeli sanathe
kuwawononga kotheratu. Solomoni anawatenga ndi kukhala akapolo
ake ogwira ntchito yathangata, monga zilili mpaka lero lino. [9] Koma
Solomoni sanagwiritse ntchito ya ukapolo Aisraeli; Iwo anali anthu ake
ankhondo, atsogoleri a ankhondo, olamulira magaleta ndi oyendetsa
magaleta ake. [10] Amenewa ndiwo anali akuluakulu oyang'anira ntchito
za mfumu Solomoni. Onse amene ankayang'anira anthu analipo 250.

[11] Solomoni anabweretsa mwana wamkazi wa Farao mu mzinda wa
Davide ku nyumba yaufumu yomwe anamumangira, pakuti iye anati,
"Mkazi wanga asakhale m'nyumba yaufumu ya Davide mfumu ya Israeli,
chifukwa malo amene Bokosi la Chipangano la Yehova lafikira ndi
opatulika."

[12] Solomoni anapereka nsembe zopsereza pa guwa lansembe la Yehova
limene anamanga patsogolo pa khonde la polowera, [13] monga momwe
zinkafunikira pa tsiku lililonse. Ankapereka nsembezo potsata malamulo
a Mose okhudza chikondwerero cha Masabata, chikondwerero cha Mwezi
Watsopano ndi zikondwerero zitatu za pa chaka: Chikondwerero cha
Buledi Wopanda yisiti, Chikondwerero cha Masabata ndi Chikondwerero
cha Misasa. [14] Potsata malangizo a Davide abambo ake, iye anayika
ansembe m'magulumagulu monga mwa ntchito zawo ndipo anayika Alevi

kukhala otsogolera matamando ndi kuthandiza ansembe pa zofunika pa tsiku lililonse. Iye anasankhanso magulumagulu a alonda a pa zipata zosiyanasiyana, chifukwa izi ndi zimene munthu wa Mulungu, Davide
analamula. 15 Anthu sanapatukepo pa zimene mfumu inalamula ansembe kapena Alevi pa china chilichonse, kuphatikiza za chuma.
16 Ntchito yonse ya Solomoni inachitika kuyambira tsiku limene maziko a Nyumba ya Mulungu anakhazikitsidwa mpaka kumaliza. Kotero Nyumba ya Yehova inamalizidwa.
17 Kenaka Solomoni anapita ku Ezioni-Geberi ndi Eloti, m'mbali mwa
nyanja ku Edomu. 18 Ndipo Hiramu anatumiza sitima zapamadzi zoyendetsedwa ndi antchito ake, antchito amene ankayidziwa bwino nyanja. Awa pamodzi ndi anthu a Solomoni, anayenda pa madzi kupita ku Ofiri ndipo anakatengako golide olemera makilogalamu 18,000 amene anabwera naye kwa mfumu Solomoni.

# 9

*Mfumu Yayikazi ya ku Seba Ichezera Solomoni*

1 Mfumu yayikazi ya ku Seba itamva za kutchuka kwa Solomoni, inabwera mu Yerusalemu kudzamuyesa ndi mafunso okhwima. Inafika ndi gulu lalikulu la ngamira zonyamula zokometsera zakudya, golide wambiri, ndi miyala yokongola. Inafika kwa Solomoni ndipo inayankhula
naye zonse zimene zinali mu mtima mwake. 2 Solomoni anayankha mafunso ake onse ndipo panalibe kanthu kalikonse kovuta kwa iye komwe
sanathe kufotokozera mfumu yayikaziyo. 3 Mfumu yayikazi ya ku Seba itaona nzeru za Solomoni komanso nyumba yaufumu imene anamanga,
4 chakudya cha pa tebulo pake, moyo wa antchito ake ndi zovala zawo; atumiki opereka zakumwa ndi zovala zawo ndiponso nsembe zopsereza zimene ankapereka ku Nyumba ya Yehova, inathedwa nzeru.
5 Iyo inati kwa mfumu, "Mbiri imene ndinamva ndili ku dziko kwathu,
ya zomwe munachita komanso nzeru zanu ndi yoona. 6 Koma sindinakhulupirire zimene ankanena mpaka nditafika ndi kuona ndi maso anga. Kunena zoona sanandiwuze ngakhale theka lomwe la kuchuluka
kwa nzeru zanu, pakuti zaposa zimene ndinamva. 7 Ngodala anthu anu! Ngodala atumiki anu amene amayimirira pamaso panu nthawi
zonse ndi kumamva nzeru zanu! 8 Atamandike Yehova Mulungu wanu amene wakondwera nanu nakukhazikani pa mpando wake waufumu kuti mulamulire m'malo mwa Yehova Mulungu wanu. Chifukwa cha chikondi cha Mulungu wanu pa Israeli, ndi khumbo lake kuti akusungeni mpaka muyaya, Iye wayika inu kukhala mfumu yawo kuti mulamulire moyenera ndi mwachilungamo."
9 Kenaka iyo inapereka kwa mfumu makilogalamu 4,000 a golide, zonunkhira zambirimbiri ndi miyala yokongola. N'kale lomwe sikunaonekenso zonunkhiritsa ngati zomwe mfumu yayikazi ya ku Seba inapereka kwa mfumu Solomoni.
10 (Anthu a Hiramu ndi anthu a Solomoni anabweretsa golide kuchokera ku Ofiri ndipo anabweretsanso mitengo ya m'bawa ndi miyala yokongola.
11 Mfumu inagwiritsa ntchito mitengo ya m'bawa pokonzera makwerero a Nyumba ya Yehova ndi nyumba yaufumu ndiponso kupangira anthu oyimba apangwe ndi azeze. Zinthu zonga zimenezi sizinaonekeponso mu Yuda).

[12] Mfumu Solomoni inapereka kwa mfumu yayikazi ya ku Seba zonse
zimene inazifuna ndi kuzipempha ndipo Solomoni anayipatsa mfumuyo
zoposa zimene iyo inabweretsa kwa Solomoni. Ndipo mfumuyo inabwer-
era ku dziko lake pamodzi ndi atumiki ake.

*Ulemerero wa Mfumu Solomoni*

[13] Kulemera kwa golide amene Solomoni amalandira pa chaka kunali
makilogalamu 23,000, [14] osawerengera amene ankabwera ndi anthu ochita
malonda ndi osinthanitsa zinthu. Komanso mafumu onse a ku Arabiya
ndi abwanamkubwa a m'dzikomo amabweretsa golide ndi siliva kwa
Solomoni.
[15] Mfumu Solomoni inapanga zishango zazikulu 200 zagolide wosas-
antha. M'chishango chilichonse mumalowa golide wolemera makilo-
galamu asanu ndi awiri. [16] Iye anapanganso zishango zing'onozing'ono
300 zagolide wosasantha ndipo chishango chilichonse chimapangidwa
ndi golide wolemera makilogalamu atatu. Mfumu inayika zishangozi
m'nyumba yaufumu yotchedwa Nkhalango ya Lebanoni.
[17] Ndipo mfumu inapanganso mpando waukulu waufumu wa nyanga
za njovu ndipo unakutidwa ndi golide woyengeka bwino. [18] Mpando wau-
fumuwo unali ndi makwerero asanu ndi limodzi ndi choyikapo mapazi
cholumikizidwa ku mpandowo. M'mbali zonse za mpandowo munali
zosanjikapo manja, ndi chifanizo cha mkango chitayima posanjikapo
manjapo. [19] Mikango khumi ndi iwiri inayimirira pa makwerero asanu ndi
imodzi aja. Umodzi mbali ina ya khwerero ndi wina mbali inayo. Palibe
mpando wonga uwu umene unapangidwapo mu ufumu wina uliwonse.
[20] Zikho zonse za mfumu Solomoni zinali zagolide, ndiponso zipangizo
zonse za ku nyumba yaufumu ya Nkhalango ya Lebanoni zinali zagolide
oyengeka bwino. Panalibe chinthu chopangidwa ndi siliva, chifukwa siliva
samayesedwa kanthu m'nthawi ya Solomoni. [21] Mfumu inali ndi sitima
zambiri zapamadzi zimene zimayendetsedwa ndi antchito a Hiramu.
Zimabwera kamodzi pa zaka zitatu zilizonse zitanyamula golide, siliva ndi
nyanga za njovu, ndiponso anyani ndi apusi.
[22] Mfumu Solomoni anapambana mafumu ena onse a dziko lapansi pa
chuma ndi nzeru. [23] Mafumu onse a dziko lapansi ankafunafuna kuonana
ndi Solomoni kuti adzamve nzeru zimene Mulungu anayika mu mtima
mwake. [24] Chaka ndi chaka, aliyense amene amabwera, amabweretsa
mphatso monga zipangizo zasiliva ndi golide, mikanjo, zida zankhondo
ndi zokometsera zakudya komanso akavalo ndi abulu.
[25] Solomoni anali ndi zipinda 4,000 zodyeramo akavalo ndi magaleta,
ndi akavalo 12,000 amene amawasunga m'mizinda yosungira magaleta
ndiponso ena anali ndi iye ku Yerusalemu. [26] Iye ankalamulira mafumu
onse kuyambira ku mtsinje wa Yufurate mpaka ku dziko la Afilisti,
kukafika ku malire a dziko la Igupto. [27] Mfumu inasandutsa siliva kukhala
wambiri ngati miyala wamba mu Yerusalemu ndipo mikungudza kukhala
yochuluka ngati mitengo ya mkuyu ya ku zigwa. [28] Solomoni ankayitanitsa
akavalo ake kuchokera ku Igupto ndi mayiko ena onse.

*Kumwalira kwa Solomoni*

[29] Tsono ntchito zina zonse za Solomoni, kuyambira pachiyambi mpaka
kumaliza, kodi sizinalembedwa m'buku la mbiri la mneneri Natani, ndi
m'buku la uneneri wa Ahiya wa ku Silo ndi m'buku la masomphenya
a mlosi Ido, lokamba za Yeroboamu mwana wa Nebati? [30] Solomoni

analamulira Aisraeli onse ku Yerusalemu zaka makumi anayi. 31 Ndipo
anamwalira nagona ndi makolo ake. Anayikidwa m'manda mu mzinda wa
Davide abambo ake. Ndipo Rehobowamu, mwana wake, analowa ufumu
m'malo mwake.

# 10

### *Aisraeli Awukira Rehobowamu*

1 Rehobowamu anapita ku Sekemu, pakuti Aisraeli onse anapita
kumeneko kuti akamulonge ufumu. 2 Yeroboamu mwana wa Nebati
atamva zimenezi (Iye anali ku Igupto, kumene anapita pothawa mfumu
Solomoni) anabwerako kuchokera ku Igupto. 3 Kotero anthu anakayitana
Yeroboamu ndipo iye ndi Aisraeli onse anapita kwa Rehobowamu ndi
kumuwuza kuti, 4 "Abambo anu anatisenzetsa goli lolemetsa koma
tsopano mutipeputsire ntchito yolemetsayi ndi goli lolemerali limene
analiyika pa ife ndipo ifeyo tidzakutumikirani."

5 Rehobowamu anayankha kuti, "Mukabwerenso pakapita masiku
atatu." Choncho anthuwo anachoka.

6 Kenaka mfumu Rehobowamu anafunsira nzeru kwa akuluakulu
amene ankatumikira abambo ake, Solomoni, pamene anali moyo. Iye
anafunsa kuti, "Kodi inu mungandilangize zotani kuti ndiwayankhe anthu
awa?"

7 Iwo anayankha kuti, "Ngati inu muwakomera mtima anthu awa ndi
kuwasangalatsa ndiponso kuwayankha mawu abwino, iwo adzakutumikirani nthawi zonse."

8 Koma Rehobowamu anakana malangizo amene akuluakulu anamupatsa
ndipo anakafunsira nzeru kwa anyamata amene anakula naye
pamodzi komanso amamutumikira. 9 Iye anawafunsa kuti, "Kodi malangizo
anu ndi otani? Kodi tiwayankhe chiyani anthu amene akunena kuti,
'Peputsani goli limene abambo anu anayika pa ife?' "

10 Anyamata amene anakula pamodzi naye anamuyankha kuti, "Anthu
amene anena kwa inu kuti, 'Abambo anu anatisenzetsa goli
lolemetsa koma inu mupeputse goli lathu,' muwawuze kuti, 'Chala
changa chaching'ono ndi chachikulu kuposa chiwuno cha abambo anga.
11 Abambo anga anakusenzetsani goli lolemetsa koma ine ndidzalichititsa
kukhala lolemetsa kwambiri. Abambo anga anakukwapulani ndi zikoti
wamba koma ine ndidzakukwapulani ndi zinkhanira.' "

12 Tsiku lachitatu Yeroboamu ndi anthu onse anabwerera kwa Rehobowamu
monga ananenera mfumu kuti, "Mukabwerenso kwa ine
pakapita masiku atatu." 13 Mfumu inawayankha mwankhanza, pokana
malangizo a akuluakulu aja. 14 Iye anatsatira malangizo a anyamata ndipo
anati, "Abambo anga anakusenzetsani goli lolemetsa koma ine ndidzalichititsa
kukhala lolemetsa kwambiri. Abambo anga anakukwapulani ndi
zikoti wamba koma ine ndidzakukwapulani ndi zinkhanira." 15 Kotero
mfumu sinamvere anthuwo, pakuti zinthu izi zinali zochokera kwa
Mulungu, kukwaniritsa mawu amene Yehova ananena kwa Yeroboamu
mwana wa Nebati kudzera mwa Ahiya wa ku Silo.

16 Aisraeli onse ataona kuti mfumu yakana kuwamvera, iwo anayankha
mfumu kuti,

"Kodi ife tili ndi gawo lanji mwa Davide,
    gawo lanji mwa mwana wa Yese?
Inu Aisraeli! Pitani kwanu.
    Iwe Davide! Yang'ana banja lako."

Kotero Aisraeli onse anapita kwawo. 17 Koma Rehobowamu anakhala
akulamulirabe Aisraeli amene amakhala m'mizinda ya Yuda.
18 Mfumu Rehobowamu inatuma Hadoramu amene ankayang'anira
ntchito yathangata, koma Aisraeli anamugenda miyala ndi kumupha.
Koma mfumu Rehobowamu anakwera galeta lake ndi kuthawira ku
Yerusalemu. 19 Motero Israeli wakhala akuwukira banja la Davide mpaka
lero lino.

# 11

1 Rehobowamu atafika ku Yerusalemu anasonkhanitsa asilikali 180,000
a fuko la Yuda ndi Benjamini kuti akachite nkhondo ndi Israeli, kuti
abwezeretse ufumu kwa Rehobowamu.
2 Koma Yehova anayankhula ndi munthu wa Mulungu Semaya kuti,
3 "Kawuze Rehobowamu mwana wa Solomoni mfumu ya Yuda ndi
Aisraeli onse ali mu Yuda ndi Benjamini kuti, 4 'Yehova akuti: Musapite
kukamenyana ndi abale anu. Pitani kwanu, aliyense wa inu, pakuti izi
ndikuchita ndine.' " Choncho anamvera mawu a Yehova ndi kubwerera
osapita kukamenyana ndi Yeroboamu.

### *Rehobowamu Akhwimitsa Chitetezo cha Yuda*

5 Rehobowamu amakhala mu Yerusalemu ndipo anamanga mizinda ya
chitetezo iyi mu Yuda: 6 Betelehemu, Etamu, Tekowa, 7 Beti Zuri, Soko,
Adulamu, 8 Gati, Maresa, Zifi, 9 Adoraimu, Lakisi, Azeka, 10 Zora, Ayaloni
ndi Hebroni. Iyi ndiye inali mizinda yotetezedwa ya Yuda ndi Benjamini.
11 Iye anakhwimitsa chitetezo cha mizindayi ndipo anayikamo atsogoleri a
ankhondo, pamodzi ndi chakudya, mafuta a olivi ndi vinyo. 12 M'mizinda
yonse anayikamo zishango zikuluzikulu ndi mikondo, ndipo anachititsa
kuti mizindayo ikhale yamphamvu. Choncho iye amalamulira Yuda ndi
Benjamini.
13 Ansembe ndi Alevi a m'madera onse a Israeli anakhala mbali ya
Rehobowamu. 14 Alevi anasiya malo awo owetera ziweto ndi katundu
wawo, ndi kubwera ku Yuda ndi ku Yerusalemu chifukwa Yeroboamu ndi
ana ake anawakana kukhala ansembe a Yehova. 15 Ndipo iye anasankha
ansembe akeake a pa malo opatulika ndi a mafano a mbuzi ndi mwana
wang'ombe amene anapanga. 16 Anthu ochokera fuko lililonse la Israeli
amene anatsimikiza mitima yawo kufunafuna Yehova Mulungu wa Israeli,
ankapitabe ku Yerusalemu kukapereka nsembe kwa Yehova, Mulungu wa
makolo awo. 17 Iwo analimbikitsa ufumu wa Yuda, ndipo anathandiza
Rehobowamu mwana wa Solomoni kwa zaka zitatu. Pa nthawi imeneyi
iye amatsatira zochita za Davide ndi Solomoni.

### *Banja la Rehobowamu*

18 Rehobowamu anakwatira Mahalati, amene abambo ake anali Yer-
imoti, mwana wa Davide, ndipo amayi ake anali Abihaili, mwana wa
Eliabu, mwana wa Yese. 19 Mkaziyo anamubereka ana aamuna awa:
Yeusi, Semariya ndi Zahamu. 20 Kenaka anakwatira Maaka, mwana
wamkazi wa Abisalomu, amene anamubereka Abiya, Atai, Ziza ndi
Selomiti. 21 Rehobowamu ankamukonda Maaka mwana wa Abisalomu
kuposa aliyense mwa akazi ake ndi azikazi. Iye anali ndi akazi 18, azikazi
60, ana aamuna 28 ndi ana aakazi 60.
22 Rehobowamu anasankha Abiya mwana wa Maaka kuti akhale
mtsogoleri pa abale ake, ndi cholinga choti adzakhale mfumu. 23 Iye

anachita mwanzeru, pomwaza ena mwa ana ake ku madera onse a Yuda
ndi Benjamini, ndi ku mizinda yonse yotetezedwa. Iye anawapatsa zinthu
zambiri ndiponso anawafunira akazi ambiri.

# 12

### *Sisaki Athira Nkhondo Dziko la Yuda*

1 Rehobowamu atakhazikika monga mfumu nakhaladi wamphamvu,
iyeyo pamodzi ndi Aisraeli onse anasiya malamulo a Yehova. 2 Chifukwa
anakhala osakhulupirika pamaso pa Yehova, Sisaki mfumu ya dziko la
Igupto inathira nkhondo Yerusalemu m'chaka chachisanu cha mfumu
Rehobowamu. 3 Sisakiyo anabwera ndi magaleta 1,200 ndi anthu okwera
akavalo 60,000 ndiponso asilikali osawerengeka ochokera ku Libiya, Suki
ndi Kusi amene anabwera naye kuchokera ku Igupto. 4 Iye analanda
mizinda yotetezedwa ya Yuda ndipo anafika mpaka ku Yerusalemu.

5 Ndipo mneneri Semaya anabwera kwa Rehobowamu ndi kwa atsogo-
leri a Yuda amene anasonkhana mu Yerusalemu chifukwa cha Sisaki ndipo
iye anawawuza kuti, "Yehova akuti, 'Inu mwandisiya, choncho Inenso
ndakusiyani ndi kukuperekani kwa Sisaki.' "

6 Atsogoleri a Israeli pamodzi ndi mfumu anadzichepetsa nati, "Yehova
ndi wolungama."

7 Yehova ataona kuti adzichepetsa, anayankhula ndi Semaya kuti,
"Pakuti adzichepetsa, Ine sindiwawononga koma posachedwapa ndiwapu-
lumutsa. Sinditsanulira ukali wanga pa Yerusalemu kudzera mwa Sisaki.
8 Komabe iwo adzakhala pansi pa ulamuliro wake, kuti aphunzire kudziwa
kusiyanitsa pakati pa kutumikira Ine ndi kutumikira mafumu a mayiko
ena."

9 Sisaki mfumu ya dziko la Igupto atathira nkhondo Yerusalemu, iye
anatenga chuma cha m'Nyumba ya Yehova ndi chuma cha m'nyumba yau-
fumu. Iye anatenga zinthu zonse kuphatikizapo zishango zagolide zimene
Solomoni anapanga. 10 Ndipo mfumu inapereka zishango zamkuwa kwa
oyang'anira m'malo mwake ndipo iwo anazipereka kwa oyang'anira
alonda amene amayang'anira pa chipata cha nyumba yaufumu. 11 Nthawi
ina iliyonse imene mfumu ikupita ku Nyumba ya Yehova, alonda amapita
nayo atanyamula zishango, ndipo kenaka amakazibwezera ku chipinda
cha alonda.

12 Pakuti mfumu Rehobowamu inadzichepetsa, mkwiyo wa Yehova
unamuchokera, sanawonongedweretu. Kunena zoona, munali zinthu zina
zabwino mu Yuda.

13 Mfumu Rehobowamu anayika maziko a ufumu wake mwamphamvu
mu Yerusalemu ndipo anapitirira kukhala mfumu. Iye anali ndi zaka 41
pamene anakhala mfumu, ndipo analamulira zaka 17 mu Yerusalemu,
mzinda wa Yehova umene anasankha pakati pa mafuko a Aisraeli mmene
Yehova anakhazikikamo. Dzina la amayi ake linali Naama, amene
anali Mwamoni. 14 Rehobowamu anachita zoyipa chifukwa mtima wake
sunafunefune Yehova.

15 Ntchito za Rehobowamu, kuyambira pachiyambi mpaka pa mapeto,
kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri la mneneri Semaya ndi mlosi Ido
amene amalemba mbiri? Panali nkhondo yosatha pakati pa Rehobowamu
ndi Yeroboamu. 16 Rehobowamu anamwalira, ndipo anayikidwa m'manda
mu mzinda wa Davide. Ndipo mwana wake Abiya analowa ufumu m'malo
wake.

# 13

*Abiya Mfumu ya Yuda*

1 M'chaka cha 18 cha ulamuliro wa Yeroboamu, Abiya analowa ufumu
wa Yuda, 2 ndipo analamulira mu Yerusalemu kwa zaka zitatu. Dzina la
amayi ake linali Maaka mwana wa Urieli wa ku Gibeya.

Koma panali nkhondo pakati pa Abiya ndi Yeroboamu. 3 Abiya
anapita ku nkhondo ndi asilikali odziwa bwino nkhondo 400,000, ndipo
Yeroboamu anandandalitsa ankhondo, asilikali 800,000 odziwa bwino
nkhondo, osankhidwa ndi amphamvu, woti amenyane naye.

4 Abiya anayima pa phiri la Zemaraimu, m'dziko lamapiri la Efereimu,
ndipo anati, "Yeroboamu ndi Aisraeli onse, tandimverani! 5 Kodi inu
simukudziwa kuti Yehova, Mulungu wa Israeli, wapereka ufumu wa
Israeli kwa Davide ndi zidzukulu zake mpaka muyaya ndiponso pangano
la mchere? 6 Komabe Yeroboamu mwana wa Nebati, mtumiki wa
Solomoni mwana wa Davide, anawukira mbuye wake. 7 Ndipo anthu ena
achabechabe anasonkhana kwa iye ndipo anatsutsana ndi Rehobowamu
mwana wa Solomoni pamene anali wamng'ono ndi wosalimba mtima ndi
wopanda mphamvu kuti athe kulimbana nawo.

8 "Ndipo tsopano inu mwakonzekera kutsutsana ndi ufumu wa Yehova,
umene uli m'manja mwa zidzukulu za Davide. Inu ndithu mulipo
ankhondo ambirimbiri ndipo muli ndi ana ang'ombe agolide amene
Yeroboamu anapanga kuti akhale milungu yanu. 9 Koma kodi inu
simunathamangitse ansembe a Yehova, ana a Aaroni ndiponso Alevi ndi
kudzisankhira ansembe anuanu monga anthu ena amachitira? Aliyense
amene amabwera kuti adzipatule atatenga mwana wang'ombe wamwa-
muna ndi nkhosa zazimuna zisanu ndi ziwiri amakhala wansembe wa
zinthu zimene sizili milungu.

10 "Koma kunena za ife, Yehova ndiye Mulungu wathu, ndipo sitina-
musiye. Ansembe amene amatumikira Yehova ndi ana a Aaroni ndipo
amathandizidwa ndi Alevi. 11 Mmawa uliwonse ndi madzulo aliwonse
amapereka nsembe zopsereza ndi kufukiza lubani kwa Yehova. Iwo
amayika buledi pa tebulo loyeretsedwa monga mwa mwambo ndipo
amayatsa nyale pa zoyikapo nyale zagolide madzulo aliwonse. Ife
timachita zofuna za Yehova Mulungu wathu. Koma inu mwamusiya.
12 Mulungu ali nafe pakuti ndiye mtsogoleri wathu. Ansembe ake
atanyamula malipenga, adzayimba mfuwu wankhondo kulimbana nanu.
Inu Aisraeli musalimbane ndi Yehova, Mulungu wa makolo anu, pakuti
simungathe kupambana."

13 Tsono Yeroboamu anali atatumiza asilikali kumbuyo mowazungulira,
kotero kuti iye ali kutsogolo kwa anthu a ku Yuda, anthu owabisalira anali
kumbuyo kwawo. 14 Asilikali a Yuda anatembenuka ndipo anaona kuti
nkhondo imachitikira kutsogolo ndi kumbuyo. Ndipo iwo anafuwulira
Yehova. Ansembe anayimba malipenga awo 15 ndipo asilikali a Yuda
anafuwula mawu ankhondo. Atafuwula mawu ankhondowo, Mulungu
anagonjetsa Yeroboamu pamodzi ndi Aisraeli onse pamaso pa Abiya ndi
Yuda. 16 Aisraeli anathawa Ayuda. Ndipo Mulungu anawapereka m'manja
mwawo. 17 Abiya pamodzi ndi anthu ake anapha anthu ambiri, kotero kuti
Aisraeli 500,000 odziwa bwino nkhondo anaphedwa. 18 Ankhondo a Israeli
anagonjetsedwa pa nthawi imeneyi, ndipo ankhondo a Yuda anapambana
chifukwa anadalira Yehova, Mulungu wa makolo awo.

19 Abiya anathamangitsa Yeroboamu ndipo anamulanda mizinda
ya Beteli, Yesana, ndi Efroni pamodzi ndi midzi yawo yozungulira.
20 Yeroboamu sanapezenso mphamvu nthawi ya Abiya. Ndipo Yehova
anamukantha nafa.
21 Koma Abiya mphamvu zake zinakula. Iye anakwatira akazi 14 ndipo
anali ndi ana aamuna 22 ndi ana aakazi 16.
22 Zina ndi zina zokhudza Abiya, zimene anachita ndi zimene
anayankhula, zinalembedwa m'buku la mbiri ya mneneri Ido.

# 14

1 Tsono Abiya anamwalira ndipo anayikidwa m'manda mu mzinda wa
Davide. Asa mwana wake anakhala mfumu m'malo mwake ndipo pa
masiku ake, dziko linakhala pa mtendere kwa zaka khumi.

### *Asa Mfumu ya Yuda*

2 Asa anachita zabwino ndi zolungama pamaso pa Yehova Mulungu
wake. 3 Iye anachotsa maguwa achilendo ndi malo opembedzerapo
mafano, anaphwanya zipilala za miyala yachipembedzo ndi kugwetsa
mafano a Asera. 4 Asa analamula Yuda kuti afunefune Yehova Mulungu wa
makolo awo ndi kumvera malamulo ndi zolamulira zake. 5 Iye anachotsa
malo opembedzera mafano ndi maguwa ofukizira lubani mu mzinda
uliwonse wa mu Yuda, ndipo mu ufumu wake munali mtendere pa nthawi
ya ulamuliro wake. 6 Asa anamanga mizinda yonse yotetezedwa ya Yuda
pakuti dziko linali pa mtendere. Panalibe amene anachita naye nkhondo
m'zaka zimenezo, pakuti Yehova anamupatsa mpumulo.
7 Iye anati kwa Yuda "Tiyeni timange mizinda iyi ndipo timange
makoma ndi nsanja, zitseko ndi zotchinga. Dzikoli likanali lathu chifukwa
tafuna Yehova Mulungu wathu; tinamufuna Iye ndipo watipatsa mpumulo
mbali zonse." Kotero iwo anamanga ndi kukhala pa ulemerero.
8 Asa anali ndi ankhondo 300,000 ochokera ku Yuda, okhala ndi
zishango zikuluzikulu ndi mikondo, ndiponso ankhondo 280,000 ochokera
ku Benjamini, okhala ndi zishango ndi mauta. Onsewa anali ankhondo
amphamvu ndi olimba mtima.
9 Zera wa ku Kusi anapita kukamenyana nawo ali ndi gulu lalikulu
kwambiri la asilikali ndi magaleta 300 ndipo anafika mpaka ku Maresa.
10 Asa anapita kukakumana naye ndipo anakhala pa mizere yawo ya
nkhondo m'chigwa cha Zefata pafupi ndi Maresa.
11 Kenaka Asa anafuwulira Yehova Mulungu wake ndipo anati "Yehova
palibe wina wofanana nanu kuti angathandize anthu opanda mphamvu
pakati pa amphamvu. Tithandizeni Inu Yehova Mulungu wathu pakuti ife
timadalira Inu ndipo m'dzina lanu ife tabwera kudzalimbana ndi gulu la
ankhondo lalikulu kwambiri ngati ili. Inu Yehova ndinu Mulungu wathu,
musalole kuti munthu akupambaneni."
12 Yehova anakantha Akusi pamaso pa Asa ndi Ayuda. Akusi anathawa,
13 ndipo Asa ndi ankhondo ake anawathamangitsa mpaka ku Gerari. Gulu
lonse lalikulu lija la Akusi linaphedwa. Sanapezeke mmodzi wamoyo
pakati pawo. Iwo anakanthidwa pamaso pa Yehova ndi asilikali ake.
Anthu a ku Yuda anatenga katundu wambiri olanda ku nkhondo. 14 Iwo
anawononga midzi yonse yozungulira Gerari pakuti mantha aakulu
wochokera kwa Yehova anagwera anthuwo. Analanda katundu wa midzi
yonse, popeza kunali katundu wambiri kumeneko. 15 Anakathiranso

nkhondo misasa ya anthu oweta ziweto ndipo anatenga nkhosa zambiri, mbuzi ndi ngamira. Atatero anabwerera ku Yerusalemu.

# 15

*Asa Akonza Chipembedzo*

1 Mzimu wa Mulungu unabwera pa Azariya mwana wa Odedi. 2 Iye
anapita kukakumana ndi Asa ndipo anati kwa iye, "Tandimverani, inu Asa ndi Ayuda onse ndi Benjamini. Yehova ali ndi inu, inunso mukakhala naye. Ngati inu mumufunafuna Iye mudzamupeza, koma ngati mumusiya,
Iye adzakusiyani. 3 Kwa nthawi yayitali Israeli anali wopanda Mulungu
weniweni, wopanda wansembe wophunzitsa ndi wopanda malamulo.
4 Koma pamene anali pa mavuto anatembenukira kwa Yehova, Mulungu
wa Israeli ndi kufunafuna Iye, ndipo anamupeza. 5 Masiku amenewo
sikunali kwabwino kuyenda ulendo, pakuti anthu onse okhala m'dziko
anali pa mavuto aakulu. 6 Mtundu umodzi umakanthidwa ndi mtundu
wina ndipo mzinda wina umakanthidwa ndi mzinda wina, pakuti Mulungu amawasautsa ndi mazunzo a mtundu uliwonse. 7 Koma inu, khalani
amphamvu ndipo musataye mtima, pakuti mudzalandira mphotho ya ntchito yanu."

8 Asa atamva mawu awa ndiponso uneneri wa Azariya mwana wa Odedi, analimba mtima. Iye anachotsa mafano onse onyansa m'dziko lonse la Yuda ndi Benjamini ndi m'mizinda yonse imene analanda a ku mapiri a Efereimu. Iye anakonzetsa guwa lansembe la Yehova limene linali kutsogolo kwa khonde la Nyumba ya Mulungu.

9 Kenaka anasonkhanitsa anthu onse a ku Yuda ndi Benjamini ndiponso anthu ochokera ku Efereimu, Manase ndi Simeoni amene ankakhala pakati pawo, pakuti gulu lalikulu linabwera kwa iye kuchokera ku Israeli litaona kuti anali ndi Yehova Mulungu wake.

10 Iwo anasonkhana mu Yerusalemu mwezi wachitatu wa chaka cha
15 cha ulamuliro wa Asa. 11 Pa nthawi imeneyi anapereka nsembe kwa
Yehova, ng'ombe 700 ndiponso nkhosa ndi mbuzi 7,000 zochokera pa
zolanda ku nkhondo zimene anabweretsa. 12 Iwo anachita pangano loti
azifunafuna Yehova, Mulungu wa makolo awo, ndi mtima ndi moyo wawo
wonse. 13 Aliyense wosafunafuna Yehova Mulungu wa Israeli aziphedwa,
kaya ndi wamng'ono kapena wamkulu, mwamuna kapena mkazi. 14 Iwo
analumbira kwa Yehova, mokweza mawu, akuyimba malipenga ndi
mbetete. 15 Anthu onse a ku Yuda anakondwera pa kulumbirako
chifukwa analumbira ndi mtima wawo wonse. Iwo anafunafuna Mulungu mwachidwi, ndipo anamupeza Iye. Kotero Yehova anawapatsa mpumulo mbali zonse.

16 Mfumu Asa anachotsanso Maaka agogo ake pa udindo wa amayi a
mfumu chifukwa anapanga fano lonyansa la Asera. Asa anagwetsa fanolo,
naliswa ndipo kenaka anakaliwotcha ku chigwa cha Kidroni. 17 Ngakhale
kuti sanachotse malo opembedzerako mafano mu Israeli, mtima wa Asa unali wodzipereka kwathunthu kwa Yehova, masiku onse a moyo wake.
18 Iye anabweretsanso m'Nyumba ya Mulungu zipangizo zasiliva, golide ndi ziwiya zina zimene iyeyo ndi abambo ake anazipatula.

19 Panalibenso nkhondo mpaka chaka cha 35 cha ufumu wa Asa.

# 16

*Zaka Zotsiriza za Asa*

1 M'chaka cha 36 cha ufumu wa Asa, Baasa mfumu ya Israeli inapita
kukathira nkhondo dziko la Yuda. Anamangira mpanda mzinda wa Rama
kuletsa aliyense kutuluka kapena kulowa m'dziko la Asa mfumu ya Yuda.
2 Ndipo Asa anatenga siliva ndi golide ku malo osungirako a m'Nyumba
ya Mulungu ndi ku nyumba yake yaufumu ndi kuzitumiza kwa Beni-
Hadadi mfumu ya Aramu imene inkakhala mu Damasiko. 3 Iye anati,
"Pakhale pangano pakati pa inu ndi ine, monga zinalili pakati pa abambo
anu ndi abambo anga. Taonani, ine ndikutumiza kwa inu siliva ndi
golide. Tsopano thetsani mgwirizano wanu ndi Baasa mfumu ya Israeli
kuti achoke kwa ine."
4 Beni-Hadadi anagwirizana ndi mfumu Asa ndipo anatumiza olamulira
nkhondo ake kukathira nkhondo mizinda ya Israeli. Iwo anagonjetsa
Iyoni, Dani, Abeli-Maimu ndi mizinda yonse yosungira chuma ya Nafutali.
5 Baasa atamva izi, anasiya kumanga Rama ndipo anayimitsa ntchito
yakeyo. 6 Ndipo mfumu Asa anabwera ndi Ayuda onse, ndipo anachotsa
miyala ndi matabwa ku Rama amene Baasa amagwiritsa ntchito. Ndi
zimenezi Asa ankamangira Geba ndi Mizipa.
7 Nthawi imeneyi mlosi Hanani anabwera kwa Asa mfumu ya Yuda
ndipo anati kwa iye, "Chifukwa chakuti munadalira mfumu ya Aramu
osati Yehova Mulungu wanu, gulu la ankhondo la mfumu ya ku Aramu
lapulumuka m'manja mwanu. 8 Kodi Akusi ndi Alibiya sanali gulu
lankhondo lamphamvu lokhala ndi magaleta ochuluka ndi okwera ma-
galeta ake? Koma pamene inu munadalira Yehova, Iye anawapereka
m'dzanja lanu. 9 Pakuti Yehova amayang'ana uku ndi uku pa dziko lonse
lapansi kuti alimbikitse iwo amene mitima yawo ayipereka kwathunthu
kwa Iye. Inu mwachita chinthu chopusa ndipo kuyambira lero mudza-
khala pa nkhondo."
10 Asa anamupsera mtima mlosi uja chifukwa cha izi mwakuti anakwiya
kwambiri namuyika m'ndende. Pa nthawi yomweyonso Asa anazunza
mwankhanza anthu ena.
11 Ntchito zina za mfumu Asa, kuyambira pachiyambi mpaka kumapeto
zalembedwa m'buku la mafumu a Yuda ndi Israeli. 12 M'chaka cha 39
cha ufumu wake, Asa anayamba kudwala nthenda ya mapazi. Ngakhale
nthendayo inali yaululu kwambiri, komabe iye sanafunefune Yehova,
koma anafuna thandizo kwa asing'anga. 13 Ndipo m'chaka cha 41 cha
ufumu wake, Asa anamwalira ndipo anayikidwa m'manda pamodzi ndi
makolo ake. 14 Iye anayikidwa m'manda amene anadzisemera yekha
mu Mzinda wa Davide. Anagoneka mtembo wake pa chithatha chimene
anayikapo zonunkhira zamitundumitundu, ndipo anasonkha chimoto
chachikulu pomuchitira ulemu.

# 17

*Yehosafati Mfumu ya Yuda*

1 Yehosafati mwana wake analowa ufumu m'malo mwake ndipo anadzil-
imbitsa pofuna kulimbana ndi Israeli. 2 Iye anayika magulu a asilikali
m'mizinda yonse yotetezedwa ya Yuda, ndipo anamanga maboma mu
Yuda ndi m'mizinda yonse ya Efereimu imene Asa abambo ake analanda.

3 Yehova anali ndi Yehosafati chifukwa m’zaka zoyambirira anatsatira
makhalidwe a Davide abambo ake. Iye sanafunsire kwa Abaala. 4 Koma
anafunafuna Mulungu wa abambo ake ndipo anatsatira malamulo ake
osati zochita za Israeli. 5 Yehova anakhazikitsa kolimba ufumuwo
m’manja mwake ndipo Ayuda onse anabweretsa mphatso kwa Yehosafati,
kotero kuti anali ndi chuma ndi ulemu wambiri. 6 Mtima wake
anawupereka kutsatira Yehova, kuwonjezera apo, anachotsa malo onse
achipembedzo ndi mafano a Asera mu Yuda.

7 M’chaka chachitatu cha ufumu wake, iye anatuma akuluakulu
ake Beni-Haili, Obadiya, Zekariya, Netaneli ndi Mikaya kukaphunzitsa
m’mizinda ya Yuda. 8 Pamodzi ndi iwo panali Alevi ena: Semaya,
Netaniya, Zebadiya, Asaheli, Semiramoti, Yonatani, Adoniya, Tobiya
ndi Tobu-Adoniya ndiponso ansembe Elisama ndi Yehoramu. 9 Iwo
anaphunzitsa mu Yuda monse atatenga Buku la Malamulo a Yehova iwo
anayenda m’mizinda yonse ya ku Yuda ndipo anaphunzitsa anthu.

10 Kuopsa kwa Yehova kunali pa maufumu onse a mayiko oyandikana
ndi Yuda, kotero kuti sanachite nkhondo ndi Yehosafati. 11 Afilisti ena
anabweretsa kwa Yehosafati mphatso ndi siliva ngati msonkho, ndipo
Aarabu anabweretsa ziweto: nkhosa zazimuna 7,700 ndi mbuzi 7,700.

12 Mphamvu za Yehosafati zinkakulirakulira. Iye anamanga malo
otetezedwa ndi mizinda yosungiramo chuma mu Yuda 13 ndipo anali ndi
katundu wambiri m’mizinda ya Yuda. Iye anayikanso asilikali odziwa
bwino nkhondo mu Yerusalemu. 14 Chiwerengero chawo potsata mabanja
awo chinali chotere:

kuchokera ku Yuda, atsogoleri a magulu 1,000;
mtsogoleri Adina, anali ndi anthu 300,000 odziwa nkhondo;
15 otsatana naye, mtsogoleri Yehohanani, anali ndi anthu 280,000;
16 otsatana naye, Amasiya mwana wa Zikiri amene anadzipereka yekha kutumikira Yehova, anali ndi anthu 200,000.
17 Kuchokera ku Benjamini:
Eliada, msilikali wolimba mtima, anali ndi anthu 200,000 amene anali ndi mauta ndi zishango;
18 otsatana naye, Yehozabadi, anali ndi anthu 180,000 okonzekera nkhondo.

19 Awa ndi anthu amene ankatumikira mfumu osawerengera amene anawayika m’mizinda yotetezedwa m’dziko lonse la Yuda.

# 18

### *Mikaya Anenera Motsutsa Ahabu*

1 Tsono Yehosafati anali ndi chuma chambiri ndi ulemu, ndipo iye
anachita mgwirizano wa ukwati ndi Ahabu. 2 Patapita zaka zina, iye
anapita kukacheza kwa Ahabu mu Samariya. Ahabu anaphera iye
pamodzi ndi anthu amene anali naye, nkhosa zambiri ndi ng’ombe
ndipo anamuwumiriza kuti akathire nawo nkhondo Ramoti Giliyadi
3 Ahabu mfumu ya Israeli anafunsa Yehosafati mfumu ya Yuda kuti, “Kodi
mudzapita nane kukalimbana ndi Ramoti Giliyadi?”

Yehosafati anayankha kuti, “Ine ndili ngati inu nomwe, ndi anthu anga
ngati anthu anu. Ife tikhala nanu limodzi pa nkhondoyi.” 4 Koma
Yehosafati anatinso kwa mfumu ya Israeli, “Choyamba mupemphe nzeru
kwa Yehova.”

5 Tsono mfumu ya Israeli inasonkhanitsa aneneri 400 ndipo inawafunsa
kuti, “Kodi tipite kukalimbana ndi Ramoti Giliyadi kapena tileke?”

Iwo anayankha kuti, “Pitani, pakuti Mulungu adzawupereka m’dzanja
la mfumu.”

6 Koma Yehosafati anafunsanso kuti, “Kodi kuno kulibe mneneri wina
wa Yehova amene ife tingafunsireko?”

7 Mfumu ya Israeli inayankha Yehosafati kuti, “Alipo munthu mmodzi
amene ife kudzera mwa iye titha kufunsira kwa Yehova, koma ndimadana
naye chifukwa sandilosera zabwino koma zoyipa nthawi zonse. Iyeyu ndi
Mikaya mwana wa Imula.”

Yehosafati anayankha kuti, “Mfumu isanene motero.”

8 Choncho mfumu ya Israeli inayitana mmodzi mwa akuluakulu ake
ndipo inati, “Kamutengeni Mikaya mwana wa Imula, abwere msanga.”

9 Mfumu ya Israeli ndi Yehosafati mfumu ya Yuda, atavala mikanjo
yawo yaufumu anali atakhala pa mipando yawo yaufumu pabwalo
lopunthira tirigu pa khomo la chipata cha Samariya, pamodzi ndi aneneri
onse akunenera pamaso pawo. 10 Tsono Zedekiya mwana wa Kenaana
anapanga nyanga zachitsulo ndipo analengeza kuti, “Yehova akuti, ‘Ndi
nyanga izi udzagunda Aaramu mpaka atawonongedwa!’ ”

11 Aneneri ena onse amanenera chimodzimodzi kuti, “Kathireni
nkhondo Ramoti Giliyadi ndipo kapambaneni, pakuti Mulungu adzamu-
pereka m’dzanja la mfumu.”

12 Wauthenga amene anapita kukayitana Mikaya anati kwa iye, “Taonani
aneneri ena onse ngati munthu mmodzi akulosera za chipambano cha
mfumu. Mawu anunso agwirizane ndi awo ndipo muyankhule zabwino.”

13 Koma Mikaya anati, “Pali Yehova wamoyo, ine ndidzanena zimene
Mulungu wanga andiwuze.”

14 Iye atafika mfumu inamufunsa kuti, “Mikaya, kodi tipite ku nkhondo
kukalimbana ndi Ramoti Giliyadi kapena tileke?”

Iye anayankha kuti, “Kathireni nkhondo ndipo kapambaneni, pakuti
mzindawo udzaperekedwa m’dzanja lanu.”

15 Mfumu inati kwa iye, “Kodi ndikuwuze kangati kuti ulumbire kuti
usandiwuze chilichonse koma zoonadi m’dzina la Yehova?”

16 Ndipo Mikaya anayankha kuti, “Ine ndinaona Aisraeli atabalalika
m’mapiri monga nkhosa zopanda m’busa, ndipo Yehova anati, ‘Anthu awa
alibe mbuye wawo. Aliyense apite kwawo mu mtendere!’ ”

17 Mfumu ya Israeli inati kwa Yehosafati, “Kodi ine sindinakuwuzeni
kuti sandinenera zabwino koma zoyipa zokhazokha?”

18 Mikaya anapitiriza ndi kunena kuti, “Imvani tsono mawu a Yehova:
Ine ndinaona Yehova atakhala pa mpando wake waufumu ndi gulu lonse
lakumwamba litayima ku dzanja lake lamanja ndi lamanzere. 19 Ndipo
Yehova anati, ‘Ndani amene adzamunyengerere Ahabu mfumu ya Israeli
kuti akathire nkhondo Ramoti Giliyadi ndi kukafera komweko?’

“Wina ananena zina, winanso ananena zina.” 20 Pomaliza mzimu wina
unatuluka ndi kuyima pamaso pa Yehova ndipo unati, “Ine ndikamunyen-
gerera!”

Yehova anafunsa kuti, “Ukagwiritsa ntchito njira yanji?”

21 Mzimuwo unati, “Ine ndidzapita ndi kukhala mzimu wabodza
m’kamwa mwa aneneri ake onse!”

Yehova anati, “ ‘Iwe ukamunyengadi iyeyo. Pita kachite zimenezo.’

22 "Choncho Yehova wayika mzimu wabodza m'kamwa mwa aneneri anuwa. Yehova waneneratu kuti inu mukaona tsoka."
23 Ndipo Zedekiya mwana wa Kenaana anapita pafupi ndi kumenya khofi Mikaya. Zedekiya anafunsa kuti, "Kodi mzimu wochokera kwa Yehova unadzera njira iti pamene unachoka kwa ine kupita kwa iwe?"
24 Mikaya anayankha kuti, "Udzadziwa pa tsiku limene uzikalowa m'chipinda cham'kati kuti ukabisale."
25 Pamenepo mfumu ya Israeli inalamula kuti, "Tengani Mikaya ndipo mupite naye kwa Amoni, wolamulira mzindawo ndi kwa Yowasi mwana
wa mfumu, 26 ndipo mukanene kuti, 'Chimene mfumu ikunena ndi ichi; Muyike munthu uyu m'ndende ndipo musamupatse kanthu kalikonse koma buledi ndi madzi pang'ono mpaka nditabwera mwamtendere.' "
27 Mikaya anayankhula kuti, "Ngati inu mukabwera mwamtendere, Yehova sanayankhule kudzera mwa ine." Ndipo anawonjeza kuti, "Anthu nonsenu, mumve zimene ndanenazi."

### *Ahabu Aphedwa ku Ramoti-Giliyadi*

28 Choncho mfumu ya Israeli ndi Yehosafati mfumu ya Yuda anapita ku
Ramoti Giliyadi. 29 Mfumu ya Israeli inati kwa Yehosafati, "Ine ndipita ku nkhondo modzibisa koma iwe uvale mikanjo yaufumu." Kotero mfumu ya Israeli inadzibisa ndipo inapita ku nkhondoko.
30 Tsono mfumu ya Aramu inalamulira olamulira magaleta kuti, "Musamenyane ndi wina aliyense, wamng'ono kapena wamkulu koma
mfumu ya Israeli yokha." 31 Olamulira magaleta ataona Yehosafati, iwo anaganiza kuti, "Mfumu ya Israeli ndi iyi." Kotero anatembenuka kukamenyana naye koma Yehosafati anafuwula, ndipo Yehova anamuthandiza.
Mulungu anawabweza m'mbuyo, 32 pakuti olamulira magaleta ataona kuti
sanali mfumu ya Israeli, anasiya kumuthamangitsa.
33 Koma munthu wina anaponya muvi wake mwachiponyeponye ndipo analasa mfumu ya Israeli pakati polumikizira malaya achitsulo. Mfumu inawuza oyendetsa galeta kuti, "Bwerera, undichotse pa nkhondo pano.
Ndavulazidwa." 34 Nkhondo inakula kwambiri tsiku lonse, ndipo mfumu
ya Israeli inakhala tsonga m'galeta lake kuyang'anana ndi Aaramu mpaka madzulo. Ndipo pamene dzuwa linkalowa inamwalira.

## 19

1 Yehosafati, mfumu ya Yuda itabwerera mwamtendere ku nyumba yake
yaufumu ku Yerusalemu, 2 mlosi Yehu, mwana wa Hanani, anatuluka kukakumana naye ndipo anati kwa mfumu, "Kodi n'koyenera kuthandiza oyipa ndi kukonda iwo amene amadana ndi Yehova? Chifukwa cha
zimenezi mkwiyo wa Yehova uli pa inu. 3 Komabe, muli zinthu zina
zabwino mwa inu, pakuti inu mwachotsa m'dziko muno mafano a Asera ndipo mwakhazikitsa mtima wanu pa kufunafuna Mulungu."

### *Yehosafati Asankha Oweruza*

4 Yehosafati anakakhala ku Yerusalemu, ndipo amayenda pakati pa anthu kuchokera ku Beeriseba mpaka ku dziko lamapiri la Efereimu
ndipo anawatembenuzira kwa Yehova, Mulungu wa makolo awo. 5 Iye
anasankha oweruza m'dzikomo, mu mzinda uliwonse wotetezedwa wa
Yuda. 6 Ndipo anawawuza kuti, "Muganize bwino zimene mukuchita, chifukwa simukuweruza m'malo mwa munthu koma Yehova, amene ali
nanu pamene mukupereka chiweruzo. 7 Tsopano kuopsa kwa Yehova

kukhale pa inu. Muweruze mosamala, pakuti ndi Yehova Mulungu wathu
palibe kupotoza chilungamo kapena kukondera kapenanso kulandira
ziphuphu.”
8 Mu Yerusalemu, Yehosafati anasankha Alevi ena, ansembe ndi at-
sogoleri a mabanja a Aisraeli kuti aziyang’anira Malamulo a Yehova
ndi kuweruza milandu. Ndipo iwo amakhala mu Yerusalemu. 9 Iye
anawalamula kuti, “Inu mutumikire mokhulupirika ndi mtima wanu
wonse moopa Yehova. 10 Pa mlandu uliwonse wobwera kwa inu
kuchokera kwa abale anu amene amakhala m’mizinda, mlandu wokhetsa
magazi kapena mlandu wosamvera malamulo kapena malangizo kapena
ziphunzitso zina, inu muziwachenjeza kuti asachimwire Yehova pakuti
mukapanda kutero mkwiyo wake udzakhala pa inu ndi abale anu. Chitani
zimenezi ndipo simudzachimwa.
11 “Amariya, mkulu wa ansembe adzakhala wokuyang’anirani pa zonse
zokhudza Yehova, ndipo Zebadiya mwana wa Ismaeli, mtsogoleri wa fuko
la Yuda, adzakhala wokuyang’anirani pa zonse zokhudza mfumu ndipo
Alevi adzatumikira ngati okuyang’anirani. Muchite molimba mtima ndipo
Yehova akhale ndi iwo amene adzachita bwino.”

# 20

*Yehosafati Agonjetsa Mowabu ndi Amoni*

1 Zitatha izi, Amowabu ndi Aamoni pamodzi ndi Ameuni ena anabwera
kudzachita nkhondo ndi Yehosafati.
2 Anthu ena anabwera kudzamuwuza Yehosafati kuti, “Gulu lalikulu
kwambiri lankhondo likubwera kudzachita nanu nkhondo lochokera ku
Edomu, ku mbali ina ya Nyanja. Gululi lafika kale ku Hazazoni Tamara”
(ndiye kuti Eni-Gedi). 3 Ndi mantha, Yehosafati anaganiza zofunsira
kwa Yehova, ndipo analengeza kuti Ayuda onse asale zakudya. 4 Anthu
a ku Yuda anabwera pamodzi kudzafuna thandizo kwa Yehova, ndipo
anabweradi kuchokera ku mzinda uliwonse wa mu Yuda kudzafunafuna
Yehova.
5 Yehosafati anayimirira pakati pa msonkhano wa Yuda ndi Yerusalemu,
pa Nyumba ya Yehova patsogolo pa bwalo latsopano 6 ndipo anati:
“Inu Yehova, Mulungu wa makolo athu, kodi Inu sindinu Mulungu
amene muli kumwamba? Inu mumalamulira maufumu onse a mi-
tundu ya anthu. Mphamvu ndi nyonga zili m’manja mwanu, ndipo
palibe amene angalimbane nanu. 7 Inu Mulungu wathu, kodi simu-
nathamangitse nzika za dziko lino pamaso pa anthu anu Aisraeli ndipo
munalipereka kwa zidzukulu za Abrahamu bwenzi lanu kwamuyaya?
8 Iwo akhala m’dzikolo ndipo anamangira Dzina lanu malo opatulika,
n’kumati, 9 ‘Ngati tsoka litigwera kaya ndi lupanga lachiweruzo, kapena
mliri, kapenanso njala, ife tidzayima pamaso panu patsogolo pa Nyumba
ya Mulungu ino imene imatchedwa ndi Dzina lanu ndipo tidzalirira kwa
inu m’masautso athu, ndipo Inu mudzatimvera ndi kutipulumutsa.’
10 “Koma tsopano pano pali anthu ochokera ku Amoni, Mowabu
ndi Phiri la Seiri amene dziko lawo Inu simunawalole Aisraeli kuti
alithire nkhondo pamene amabwera kuchokera ku Igupto. Kotero
anatembenuka ndi kuwaleka ndipo sanawawononge. 11 Taonani,
mmene akutibwezera ife pobwera kudzatithamangitsa m’dziko limene
inu munatipatsa ngati cholowa chathu. 12 Inu Mulungu wathu, kodi
simuwaweruza? Pakuti ife tilibe mphamvu zolimbana ndi gulu lalikulu

lankhondo limene likutithira nkhondoli. Ife sitikudziwa choti tichite,
koma maso athu ali pa Inu."

13 Anthu onse a Yuda, pamodzi ndi akazi awo ndi ana ndi makanda,
anayima chilili pamaso pa Yehova.

14 Ndipo Mzimu wa Yehova unabwera pa Yahazieli mwana wa Zekariya,
mwana wa Benaya, mwana wa Yeiyeli, mwana wa Mataniya Mlevi,
chidzukulu cha Asafu, atayimirira mu msonkhano.

15 Iye anati, "Tamverani mfumu Yehosafati ndi onse amene amakhala
mu Yuda ndi Yerusalemu! Zimene Yehova akunena kwa inu ndi izi:
'Musaope kapena kutaya mtima chifukwa cha gulu lalikulu lankhondo
ili. Pakuti nkhondoyi si yanu, koma ya Mulungu. 16 Mawa mupite
mukamenyane nawo. Adzakhala akubwera mokweza kudzera Njira ya
Zizi, ndipo mukawapeza kumapeto kwa chigwa cha ku chipululu cha
Yeruweli. 17 Sikudzafunika kuti Inu mumenyane nawo pa nkhondo
imeneyi. Inu mukhale pa malo anu; imani molimba ndipo onani
chipulumutso chimene Yehova adzakupatsani, Inu Yuda ndi Yerusalemu.
Musaope, musataye mtima. Pitani kuti mukakumane nawo mawa, ndipo
Yehova adzakhala nanu.' "

18 Yehosafati anaweramitsa nkhope yake ndi kugunda pansi, ndiponso
anthu onse a Yuda ndi Yerusalemu anagwa pansi ndi kulambira Yehova.
19 Kenaka Alevi ena ochokera ku mabanja a Kohati ndi Kora anayimirira
ndipo anatamanda Yehova Mulungu wa Israeli ndi mawu ofuwula
kwambiri.

20 Mmamawa, ananyamuka kupita ku chipululu cha Tekowa. Akun-
yamuka, Yehosafati anayimirira ndipo anati, "Tandimverani ine anthu
a Yuda ndi Yerusalemu! Khalani ndi chikhulupiriro mwa Yehova Mu-
lungu wanu ndipo mudzatchinjirizidwa, khalani ndi chikhulupiriro mwa
aneneri ake ndipo mudzapambana." 21 Atafunsira kwa anthu, Yehosafati
anasankha anthu oti ayimbire Yehova ndi kumutamanda chifukwa cha
ulemerero wa chiyero chake pamene amapita ali patsogolo pa gulu la
ankhondo, akunena kuti:

"Yamikani Yehova
    pakuti chikondi chake ndi chosatha."

22 Atangoyamba kuyimba ndi kutamanda, Yehova anapereka m'manja
mwawo anthu a ku Amoni ndi a ku Mowabu ndiponso a ku Phiri la Seiri
amene amalimbana ndi Yuda, ndipo anagonjetsedwa. 23 Anthu a ku Amoni
ndi a ku Mowabu anawukira anthu ochokera ku Phiri la Seiri, ndipo
anawawononga ndi kuwatheratu. Atatsiriza kuwapha anthu ochokera ku
Seiri anamenyana wina ndi mnzake mpaka kuwonongana.

24 Anthu a ku Yuda atafika pa malo oyang'anana ndi chipululu ndi
kuona kumene kunali gulu lalikulu lankhondo, iwo anangoona mitembo
yokhayokha itagona pansi ndipo palibe amene anathawa. 25 Choncho
Yehosafati ndi anthu ake anapita kukafunkha, ndipo pakati pawo anapeza
katundu wambiri ndi zovala ndiponso zinthu zina zamtengowapatali
kuposa zomwe akanatha kunyamula. Kunali katundu wambiri kotero
kuti zinawatengera masiku atatu kuti amutenge. 26 Tsiku lachinayi ana-
sonkhana ku chigwa cha Beraka kumene anatamanda Yehova. N'chifukwa
chake malowa amatchedwa chigwa cha Beraka mpaka lero.

27 Tsono motsogozedwa ndi Yehosafati, anthu onse a Yuda ndi
Yerusalemu anabwerera ku Yerusalemu mokondwera pakuti Yehova
anawagonjetsera adani awo. 28 Iwo analowa mu Yerusalemu ndipo
anapita ku Nyumba ya Mulungu akuyimba azeze, apangwe ndi malipenga.

29 Kuopsa kwa Mulungu kunali pa maufumu onse a mayiko amene
anamva mmene Yehova anamenyera adani a Aisraeli. 30 Ndipo ufumu wa
Yehosafati unali pa mtendere pakuti Mulungu wake anamupatsa mpumulo
ku mbali zonse.

### *Kutha kwa Ufumu wa Yehosafati*

31 Choncho Yehosafati analamulira Yuda. Iye anali wa zaka 35 pamene
anakhala mfumu ya Yuda ndipo analamulira mu Yerusalemu kwa zaka
25. Dzina la amayi ake linali Azuba mwana wa Sili. 32 Iye ankayenda
m'njira za Asa abambo ake ndipo sanapatuke pa zimenezi pakuti anachita
zolungama pamaso pa Yehova. 33 Komabe malo opembedzerapo mafano
sanachotsedwe ndipo anthu sanaperekebe mitima yawo kwa Mulungu wa
makolo awo.
34 Zochitika zina zokhudza ufumu wa Yehosafati, kuyambira pachiyambi
mpaka pa mapeto, zalembedwa m'buku la Yehu mwana wa Hanani,
zomwe zikupezeka m'buku la mbiri ya mafumu a Israeli.
35 Zitapita izi, Yehosafati mfumu ya Yuda inachita mgwirizano ndi
Ahaziya mfumu ya Israeli, amene anachita zoyipa kwambiri. 36 Iye
anagwirizana ndi Ahaziya kuti apange sitima zapamadzi zochitira mal-
onda. Atazipanga zimenezi ku Ezioni-Geberi, 37 Eliezara mwana wa
Dodavahu wa ku Maresa ananenera motsutsana ndi Yehosafati ndipo
anati, "Chifukwa chakuti wachita mgwirizano ndi Ahaziya, Yehova adza-
wononga zimene mwapangazo!" Sitima za pamadzizo zinawonongeka
ndipo sizinapite n'komwe kumene zimakachita malonda.

## 21

1 Yehosafati anamwalira nayikidwa m'manda pamodzi ndi makolo ake
mu mzinda wa Davide. Ndipo Yehoramu mwana wake analowa ufumu
m'malo mwake. 2 Abale ake a Yehoramu, ana aamuna a Yehosafati, anali
Azariya, Yehieli, Zekariya, Azariyahu, Mikayeli ndi Sefatiya. Onsewa anali
ana a Yehosafati mfumu ya Israeli. 3 Abambo awo anawapatsa mphatso
zambiri za siliva, golide ndi zinthu zina zamtengowapatali komanso
mizinda yotetezedwa ya Yuda. Koma iye anapereka ufumu kwa Yehoramu
chifukwa anali mwana wake woyamba kubadwa.

### *Yehoramu Mfumu ya Yuda*

4 Yehoramu atakhazikika pa ufumu wa abambo ake, iye anapha abale
ake ndi lupanga pamodzi ndi atsogoleri ena a Israeli. 5 Yehoramu anali
wa zaka 32 pamene anakhala mfumu, ndipo analamulira mu Yerusalemu
zaka zisanu ndi zitatu. 6 Iye anayenda m'njira za mafumu a Israeli,
monga mmene linachitira banja la Ahabu, pakuti anakwatira mwana wa
Ahabu. Ndipo anachita zoyipa pamaso pa Yehova. 7 Komabe, chifukwa cha
pangano limene Yehova anachita ndi Davide, Yehova sanafune kuwononga
banja la Davide. Iye analonjeza kusungira nyale Davide ndi zidzukulu zake
mpaka muyaya.
8 Pa nthawi ya Yehoramu, Edomu anawukira Yuda ndipo anadzisankhira
mfumu. 9 Choncho Yehoramu anapita kumeneko pamodzi ndi atsogoleri
ake ndi magaleta ake onse. Aedomu anamuzungulira pamodzi ndi
atsogoleri ake koma iye ananyamuka ndi kuthawa usiku. 10 Mpaka lero
lino Edomu ndi wowukira ulamuliro wa Yuda.
Pa nthawi yomweyi, mzinda wa Libina unawukiranso chifukwa Yeho-
ramu anasiya Yehova, Mulungu wa makolo ake. 11 Iye anamanganso malo

opembedzerapo mafano m'mapiri a Yuda ndipo anachititsa anthu a mu Yerusalemu kukhala osakhulupirika. Choncho anasocheretsa anthu a ku Yuda.
12 Yehoramu analandira kalata yochokera kwa mneneri Eliya yonena kuti,
"Yehova Mulungu wa Davide abambo ako akuti, 'Iwe sunayende m'njira ya Yehosafati abambo ako kapena Asa mfumu ya Yuda. 13 Koma
wayenda m'njira za mafumu a Israeli ndipo watsogolera anthu a ku Yuda ndi Yerusalemu kukhala osakhulupirika, monga linachitira banja la Ahabu. Waphanso abale ako, abale a banja la abambo ako,
anthu amene anali abwino kuposa iweyo. 14 Kotero tsono Yehova ali
pafupi kukantha anthu ako, ana ako, akazi ako ndi zinthu zako zonse,
ndi chilango chachikulu. 15 Ndipo iwe udzadwala nthenda yoopsa
yam'mimba, mpaka nthendayo idzachititsa matumbo ako kutuluka.' "
16 Yehova anamuutsira Yehoramuyo mkwiyo wa Afilisti ndi Aarabu
amene amakhala pafupi ndi Akusi. 17 Iwo anathira nkhondo Yuda.
Analowanso ndi kutenga katundu yense amene anamupeza m'nyumba ya mfumu pamodzi ndi ana ake ndi akazi ake. Palibe mwana amene anatsala kupatula mwana wake wamng'ono kwambiri, Ahaziya.
18 Izi zonse zitachitika, Yehova anakantha Yehoramu ndi nthenda
yam'mimba imene inali yosachiritsika. 19 Patapita nthawi, kumapeto
kwa chaka chachiwiri, matumbo ake anatuluka chifukwa cha nthendayo, ndipo anafa imfa yopweteka kwambiri. Anthu ake sanasonkhe moto kumuchitira ulemu, monga anachitira ndi makolo ake.
20 Yehoramu anali wa zaka 32 pamene anakhala mfumu. Iyeyo analamulira mu Yerusalemu zaka zisanu ndi zitatu. Ndipo anamwalira popanda odandawula, nayikidwa m'manda mu mzinda wa Davide, koma osati m'manda a mafumu.

# 22

*Ahaziya Mfumu ya Yuda*

1 Anthu a mu Yerusalemu anayika Ahaziya mwana wamng'ono kwambiri wa Yehoramu kukhala mfumu m'malo mwake, popeza gulu lankhondo limene linabwera ndi Aarabu ku misasa, linapha ana onse aakulu. Motero Ahaziya mwana wa Yehoramu mfumu ya Yuda anayamba kulamulira.
2 Ahaziya anali wa zaka 22 pamene anakhala mfumu ndipo analamulira mu Yerusalemu chaka chimodzi. Dzina la amayi ake linali Ataliya, chidzukulu cha Omuri.
3 Nayenso anayenda m'njira ya banja la Ahabu, pakuti amayi ake
anamulimbikitsa kuchita zolakwika. 4 Iye anachita zoyipa pamaso pa
Yehova monga momwe banja la Ahabu linachitira, pakuti atamwalira abambo ake, iwo anakhala alangizi ake, kumene kunali kudziwononga
kwake. 5 Iyeyo anatsatiranso uphungu wawo pamene anapita ndi
Yehoramu, mwana wa Ahabu, mfumu ya Israeli kukachita nkhondo ndi Hazaeli mfumu ya Aramu ku Ramoti Giliyadi. Aaramu anavulaza
Yehoramu, 6 kotero iye anabwerera ku Yezireeli kuti akachire mabala
amene anamuvulaza ku Ramoti pa nkhondo ndi Hazaeli mfumu ya Aaramu.
Ndipo Ahaziya, mwana wa Yehoramu mfumu ya Yuda anapita ku Yezireeli kukaona Yehoramu mwana wa Ahabu chifukwa anavulazidwa.

7 Mulungu anakonza kuti Ahaziya akaphedwe pa ulendo wake
wokacheza. Ahaziya atafika, iye ndi Yoramu anapita kukakumana ndi
Yehu mwana wa Nimisi, amene Yehova anamudzoza kuti akawononge
banja la Ahabu. 8 Pamene Yehu ankalanga banja la Ahabu anapeza
atsogoleri a ku Yuda ndiponso ana aamuna a abale ake a Ahaziya amene
amatumikira Ahaziya, ndipo anawapha. 9 Kenaka anapita kukafunafuna
Ahaziya, ndipo anthu ake anagwira Ahaziya pamene amabisala mu
Samariya. Anabwera naye kwa Yehu ndipo anaphedwa. Iwo anamuyika
m'manda, pakuti anati, "Iyeyu anali mwana wa Yehosafati amene anafu-
nafuna Yehova ndi mtima wake wonse." Kotero panalibe wamphamvu
m'banja la Ahaziya kuti n'kukhala mfumu.

### *Ataliya ndi Yowasi*

10 Ataliya, amayi ake a Ahaziya, ataona kuti mwana wawo wafa,
ananyamuka nakapha onse a banja laufumu la Yuda. 11 Koma Yehoseba,
mwana wamkazi wa mfumu Yehoramu, anatenga Yowasi mwana wa
Ahaziya, momuba ndi kumuchotsa pakati pa ana aamuna a mfumu
amene amati aphedwe ndipo anamuyika iye ndi mlezi wake m'chipinda
chogona. Motero Yehoseba, mwana wamkazi wa mfumu Yehoramu,
mkazi wa wansembe Yehoyada, yemwe anali mlongo wake wa Ahaziya
anamubisa mwanayo kuti Ataliya asamuphe. 12 Mwanayo anakhala
mobisala pamodzi ndi iwo mu Nyumba ya Mulungu kwa zaka zisanu ndi
chimodzi muulamuliro wa Ataliya.

## 23

1 M'chaka chachisanu ndi chiwiri Yehoyada anaonetsa mphamvu zake.
Iye anachita pangano ndi olamulira magulu a anthu 100: Azariya
mwana wa Yerohamu, Ismaeli mwana wa Yehohanani, Azariya mwana
wa Obedi, Maaseya mwana wa Adaya ndi Elisafati mwana wa Zikiri.
2 Iwo anayendayenda m'dziko la Yuda ndipo anasonkhanitsa Alevi ndi
atsogoleri a mabanja a Aisraeli ochokera m'mizinda yonse. Atabwera
ku Yerusalemu, 3 msonkhano wonse unachita pangano ndi mfumu mu
Nyumba ya Mulungu.
Yehoyada anawawuza kuti, "Mwana wa mfumu adzalamulira monga
ananenera Yehova zokhudza ana a Davide. 4 Tsopano zimene muti
muchite ndi izi: Limodzi mwa magawo atatu a ansembe ndi Alevi amene
mudzakhale pa ntchito pa Sabata muzikalondera pa khomo, 5 ndi limodzi
la magawo atatu likakhale ku nyumba yaufumu ndipo limodzi la magawo
atatu likakhale ku chipata cha Maziko ndipo anthu ena onse akakhale
m'mabwalo a Nyumba ya Yehova. 6 Musalole aliyense kulowa m'Nyumba
ya Yehova kupatula ansembe ndi Alevi amene akutumikira. Iwo atha
kutero chifukwa apatulidwa koma anthu ena onse ayenera kumvera
zimene Yehova walamula. 7 Alevi akhale mozungulira mfumu, munthu
aliyense ali ndi chida chake m'manja. Aliyense amene alowe m'Nyumba
ya Mulungu ayenera kuphedwa. Mukhale nayo pafupi mfumu kulikonse
kumene izipita."
8 Alevi ndi anthu onse a ku Yuda anachita monga momwe wansembe
Yehoyada anawalamulira. Aliyense anatenga anthu ake amene ankagwira
ntchito pa Sabata ndi amene amapita kukapuma, pakuti wansembe
Yehoyada sanalole gulu lililonse kuti lipite. 9 Ndipo Yehoyada anapereka
kwa atsogoleri a magulu a anthu 100 mikondo ndi zishango zazikulu ndi
zazing'ono zimene zinali za Davide ndipo zinali m'Nyumba ya Mulungu.

10 Iye anayika anthu onse, aliyense ali ndi chida m'dzanja lake mozun-
gulira mfumu pafupi ndi guwa ndi Nyumba ya Mulungu, kuyambira mbali
ya kummwera mpaka kumpoto kwa Nyumba ya Mulungu.

11 Yehoyada ndi ana ake anatulutsa mwana wa mfumu ndipo ana-
mumveka chipewa chaufumu ndipo anamupatsa Buku la Chipangano
namulonga ufumu. Yehoyada ndi ana ake anamudzoza ndipo anafuwula
kuti, "Ikhale ndi moyo wautali mfumu!"

12 Ataliya atamva phokoso la anthu akuthamanga ndi kukondwerera
mfumu, anapita ku Nyumba ya Yehova komwe kunali anthuko. 13 Iye
anayang'ana, ndipo anaona mfumu itayima pa chipilala chake cha-
pakhomo. Atsogoleri ndi oyimba malipenga anali pafupi ndi mfumuyo,
ndipo anthu onse a m'derali amakondwerera ndi kuyimba malipenga
ndiponso oyimba ndi zida amatsogolera matamando. Pamenepo Ataliya
anang'amba mkanjo wake ndipo anafuwula kuti, "Kuwukira! Kuwukira!"

14 Wansembe Yehoyada anatumiza olamulira magulu a anthu 100
aja, amene amayang'anira asilikali ndipo anawawuza kuti, "Mutulutseni
ameneyu pakati pa mizere yanu ndipo muphe aliyense amene adzamut-
sata." Pakuti ansembe anati, "Musamuphere m'Nyumba ya Mulungu wa
Yehova," 15 choncho anamugwira pamene amafika pa chipata cha Kavalo
pa bwalo la nyumba yaufumu, ndipo anamuphera pamenepo.

16 Tsono Yehoyada anachita pangano, iye mwini ndi anthu onse
ndiponso mfumu kuti adzakhala anthu a Yehova. 17 Anthu onse anapita
ku kachisi wa Baala ndipo anamugwetsa. Iwo anaphwanya maguwa ndi
mafano ndi kupha Matani wansembe wa Baala patsogolo pa maguwawo.

18 Kenaka Yehoyada anayika ansembe, omwe anali Alevi kukhala
oyang'anira Nyumba ya Yehova, amene Davide anawapatsa ntchito
yoti azipereka nsembe zopsereza kwa Yehova m'Nyumba ya Mulungu,
monga zinalembedwa m'malamulo a Mose kuti azitero akukondwera ndi
kuyimba monga Davide analamulira. 19 Ndipo anayika alonda a pa khomo
pa zipata za Nyumba ya Yehova kuti aliyense amene ndi odetsedwa
asalowe.

20 Iye anatenga olamulira magulu a anthu 100, anthu otchuka, olamulira
anthu ndi anthu onse a m'deralo ndipo anabweretsa mfumu kuchokera
ku Nyumba ya Mulungu. Iwo anapita ku nyumba yaufumu kudzera
ku Chipata Chakumitu ndipo anayikira mfumu mpando wolemekezeka,
21 ndipo anthu onse a m'derali anakondwera. Tsono mu mzinda munali
bata chifukwa Ataliya anaphedwa ndi lupanga.

# 24

*Yowasi Akonzanso Nyumba ya Mulungu*

1 Yowasi anali wa zaka zisanu ndi ziwiri pamene anakhala mfumu,
ndipo analamulira mu Yerusalemu kwa zaka makumi anayi. Dzina la
amayi ake linali Zibiya wa ku Beeriseba. 2 Yowasi anachita zolungama
pamaso pa Yehova nthawi yonse ya moyo wa wansembe Yehoyada.
3 Yehoyada anamupezera iye akazi awiri, ndipo anabereka ana aamuna
ndi aakazi.

4 Patapita nthawi Yowasi anatsimikiza zokonzanso Nyumba ya Yehova.
5 Iye anayitanitsa pamodzi ansembe ndi Alevi ndipo anawawuza kuti,
"Pitani ku mizinda ya Yuda ndi kukasonkhetsa ndalama za pa chaka kwa

Aisraeli onse zokonzera Nyumba ya Mulungu wanu. Chitani zimenezi
tsopano." Koma Alevi sanachite zimenezi mwachangu.

6 Choncho mfumu inayitanitsa Yehoyada, mkulu wa ansembe ndipo inati
kwa iye, "Kodi n'chifukwa chiyani simunawuze Alevi kuti asonkhetse
ndalama ku Yuda ndi Yerusalemu, msonkho umene anakhazikitsa Mose
mtumiki wa Yehova ndiponso gulu lonse la Aisraeli mu tenti yaumboni?"

7 Ana a mkazi woyipa, Ataliya, anathyola chitseko cha Nyumba ya
Mulungu ndipo anagwiritsa ntchito zinthu zopatulika popembedza Baala.

8 Mfumu italamulira, bokosi linapangidwa ndipo linayikidwa panja pa
chipata cha Nyumba ya Yehova. 9 Ndipo analengeza kwa anthu a mu Yuda
ndi mu Yerusalemu kuti abweretse kwa Yehova msonkho umene Mose
mtumiki wa Mulungu analamulira Aisraeli m'chipululu. 10 Akuluakulu
onse ndi anthu onse anabweretsa zopereka zawo mokondwera ndipo
anaziponya m'bokosi mpaka linadzaza. 11 Nthawi ina iliyonse imene
Alevi abweretsa bokosilo kwa akuluakulu a mfumu ndipo akaona kuti
muli ndalama zambiri, mlembi waufumu ndi nduna yayikulu ya mkulu
wa ansembe amabwera ndi kuchotsa ndalama m'bokosi muja ndipo
amalitenga kukaliyika pamalo pake. Iwo amachita izi nthawi ndi nthawi
ndipo anapeza ndalama zambiri. 12 Mfumu pamodzi ndi Yehoyada
anapereka ndalamazo kwa anthu oyang'anira ntchito ku Nyumba ya
Yehova. Analemba ntchito amisiri a miyala ndi a matabwa kuti akonzenso
Nyumba ya Yehova. Analembanso ntchito amisiri a zitsulo ndi mkuwa kuti
akonze Nyumba ya Mulungu.

13 Anthu amene ankagwira ntchito anali odziwa bwino, ndipo ntchi-
toyo inagwiridwa bwino ndi manja awo. Iwo anamanganso Nyumba
ya Mulungu motsatira mapangidwe ake oyamba ndipo anayilimbitsa.
14 Atamaliza, iwo anabweretsa ndalama zotsala kwa mfumu ndi Yehoyada,
ndipo anazigwiritsira ntchito popangira zida za m'Nyumba ya Yehova:
ziwiya zogwiritsa ntchito potumikira ndi popereka nsembe zopsereza,
komanso mbale ndi ziwiya zagolide ndi siliva. Nthawi yonse ya moyo
wa Yehoyada, nsembe zopsereza zinkaperekedwa mosalekeza m'Nyumba
ya Yehova.

15 Tsono Yehoyada anakalamba ndipo anali ndi zaka zambiri. Pambuyo
pake iye anamwalira ali ndi zaka 130. 16 Iyeyo anayikidwa m'manda
pamodzi ndi mafumu mu mzinda wa Davide chifukwa cha zabwino
zimene anachita mu Israeli, kuchitira Mulungu ndi Nyumba yake.

### *Kuyipa kwa Yowasi*

17 Atamwalira Yehoyada, akuluakulu a Yuda anabwera kudzapereka
ulemu kwa mfumu, ndipo mfumu inawamvera. 18 Iwo anasiya Nyumba ya
Yehova, Mulungu wa makolo awo ndipo anapembedza Asera ndi mafano.
Chifukwa cha kulakwa kwawo, mkwiyo wa Yehova unabwera pa Yuda ndi
Yerusalemu. 19 Ngakhale Yehova anatumiza aneneri kwa anthuwo kuti
awabweze kwa Iye, ngakhale aneneri ananenera mowatsutsa, anthuwo
sanamvere.

20 Kenaka Mzimu wa Mulungu unabwera pa Zekariya mwana wa
wansembe Yehoyada. Iye anayimirira pamaso pa anthu ndipo anati,
"Zimene Mulungu akunena ndi Izi: 'Chifukwa chiyani simukumvera
Malamulo a Yehova? Simudzapindula. Chifukwa mwasiya Yehova, Iyenso
wakusiyani.' "

21 Koma anthuwo anamuchitira chiwembu molamulidwa ndi mfumu
ndipo anamugenda miyala ndi kumupha m'bwalo la Nyumba ya Mulungu.

22 Mfumu Yowasi sinakumbukire zabwino zimene Yehoyada abambo ake
a Zekariya anamuchitira, koma anapha mwana wake. Pamene amafa, iye
ananena kuti, “Yehova aone zimenezi ndipo abwezere chilango.”
23 Pakutha kwa chaka, gulu lankhondo la Aramu linadzamenyana ndi
Yowasi. Linalowa mu Yuda ndi mu Yerusalemu ndi kupha atsogoleri
onse a anthu. Zonse zimene analanda anazitumiza kwa mfumu ya ku
Damasiko. 24 Ngakhale kuti gulu lankhondo la Aramu linabwera ndi
anthu ochepa okha, Yehova anapereka m’manja mwawo gulu lalikulu
lankhondo. Chifukwa Yuda anasiya Yehova Mulungu wa makolo awo,
chiweruzo chinachitika pa Yowasi. 25 Pamene Aaramu amachoka, anasiya
Yowasi atavulazidwa kwambiri. Akuluakulu ake anamuchitira chiwembu
chifukwa anapha mwana wa wansembe Yehoyada, ndipo anamupha ali
pa bedi pake. Choncho anafa ndipo anayikidwa m’manda mu mzinda wa
Davide, koma osati manda a mafumu.
26 Iwo amene anamuchitira chiwembu anali Zabadi mwana wa Simeati,
mkazi wa ku Amoni, ndi Yehozabadi mwana wa Simiriti, mkazi wa ku
Mowabu. 27 Za ana ake aamuna, uneneri wonena za iye, mbiri ya
kumanganso Nyumba ya Mulungu, zalembedwa m’buku lofotokoza za
mafumu. Ndipo Amaziya mwana wake analowa ufumu m’malo mwake.

# 25

*Amaziya Mfumu ya Yuda*

1 Amaziya anali wa zaka 25 pamene anakhala mfumu, ndipo anala-
mulira mu Yerusalemu kwa zaka 29. Dzina la amayi ake linali Yehoyadini
wa ku Yerusalemu. 2 Iye anachita zolungama pamaso pa Yehova, koma
osati ndi mtima wonse. 3 Pamene mphamvu zonse zaufumu zinali
m’manja mwake, iye anapha akuluakulu amene anapha abambo ake,
mfumu ija. 4 Komabe iye sanaphe ana awo koma anatsatira zolembedwa
m’buku la Mose, m’mene Yehova analamula kuti, “Makolo sadzaphedwa
chifukwa cha ana awo kapena ana kuphedwa chifukwa cha makolo awo.
Aliyense adzafera machimo ake.”
5 Amaziya anasonkhanitsa anthu a ku Yuda ndipo anawapatsa zochita
molingana ndi mabanja awo kukhala anthu olamulira 1,000, ndi olamulira
100 pa Ayuda onse ndi Benjamini. Ndipo iye anawerenga amene anali
ndi zaka makumi awiri kapena kupitirirapo napeza kuti analipo amuna
300,000 okonzeka kugwira ntchito ya usilikali, okhoza kugwiritsa ntchito
mkondo ndi chishango. 6 Iye analembanso ntchito anthu odziwa nkhondo
100,000 ochokera ku Israeli pa mtengo wa makilogalamu 3,400 a siliva.
7 Koma munthu wa Mulungu anabwera kwa iye ndipo anati, “Inu
mfumu, asilikali awa ochokera ku Israeli asapite ndi inu, pakuti Yehova
sali ndi Israeli kapena ndi aliyense wa anthu a Efereimu. 8 Ngakhale
mupite ndi kuchita nkhondo molimba mtima, Mulungu adzakugonjetsani
pamaso pa adani anu, pakuti Mulungu ali ndi mphamvu yothandiza
kapena kugonjetsa.”
9 Amaziya anafunsa munthu wa Mulungu kuti, “Koma nanga za
makilogalamu aja a siliva amene ndapereka kwa asilikali a Israeli?”
Munthu wa Mulungu anayankha kuti, “Yehova atha kukupatsani
zambiri kuposa zimenezo.”
10 Choncho Amaziya anachotsa asilikali amene anabwera kwa iye
kuchokera ku Efereimu ndipo anawatumiza kwawo. Iwo anakwiyira
anthu a ku Yuda ndipo anapita kwawo atapsa mtima kwambiri.

11 Ndipo Amaziya analimba mtima ndipo anatsogolera gulu lake
lankhondo ku Chigwa cha Mchere, kumene anapha anthu 10,000 a ku Seiri.
12 Gulu la ankhondo la Yuda linagwiranso anthu amoyo 10,000, napita
nawo pamwamba pa thanthwe ndipo anawaponya pansi kotero kuti onse
ananyenyeka.

13 Pa nthawi imeneyi asilikali amene Amaziya anawabweza ndipo
sanawalole kuti achite nawo nkhondo, anakathira nkhondo mizinda ya
Yuda kuyambira ku Samariya mpaka ku Beti-Horoni. Iwo anapha anthu
3,000 ndipo anafunkha katundu wambiri.

14 Amaziya atabwerera kuja anakapha Aedomu, anabweretsa milungu
ya anthu a ku Seiri. Ndipo anayika kuti ikhale milungu yake, ankayipem-
bedza ndi kupereka nsembe zopsereza. 15 Yehova anakwiyira Amaziya,
ndipo anamutumizira mneneri amene anati, "N'chifukwa chiyani muku-
pembedza milungu ya anthu awa, imene sinathe kupulumutsa anthu ake
m'dzanja lanu?"

16 Iye ali kuyankhula, mfumu inati, "Kodi ife takusankha iwe kuti ukhale
mlangizi wa mfumu? Khala chete! Ufuna kuphedweranji?"

Choncho mneneriyo analeka koma anati, "Ine ndikudziwa kuti Mulungu
watsimikiza kukuwonongani chifukwa mwachita izi ndipo simunamvere
uphungu wanga."

17 Amaziya mfumu ya ku Yuda, atafunsa alangizi ake, anatumiza mawu
awa kwa Yowasi mwana wa Yehowahazi mwana wa Yehu, mfumu ya
Israeli: "Bwera udzakumane nane maso ndi maso."

18 Koma Yowasi mfumu ya Israeli inayankha Amaziya mfumu ya
Yuda kuti, "Nthawi ina kamtengo kaminga ka ku Lebanoni kanatumiza
mawu kwa mkungudza wa ku Lebanoni kuti, 'Pereka mwana wako
wamkazi kwa mwana wanga kuti amukwatire!' Koma chirombo cha ku
Lebanoni chinabwera ndi kupondaponda mtengo wa minga uja. 19 Iwe
ukuti wagonjetsa Edomu, ndipo tsopano ukudzikuza ndi kudzitamandira,
koma khala kwanu komweko! N'chifukwa chiyani ukufuna mavuto ndi
kudzichititsa kuti ugwe pamodzinso ndi Yuda?"

20 Komabe Amaziya sanamvere pakuti ndi Mulungu amene anakonzer-
atu kuti awapereke kwa Yehowasi, chifukwa iwo amapembedza milungu
ya ku Edomu. 21 Kotero Yowasi mfumu ya Israeli inakamuthira nkhondo.
Iye ndi Amaziya anayang'anana maso ndi maso ku Beti-Semesi ku Yuda.
22 Yuda anagonjetsedwa ndi Israeli ndipo munthu aliyense anathawira
kwawo. 23 Yehowahazi mfumu ya Israeli inagwira Amaziya mfumu ya
Yuda, mwana wa Yowasi, mwana wa Ahaziya ku Beti-Semesi. Yehowasi
anabwera naye ku Yerusalemu ndipo anagwetsa khoma la Yerusalemu
kuyambira pa Chipata cha Efereimu mpaka ku Chipata Chapangodya,
khoma lotalika mamita 180. 24 Iye anatenga golide ndi siliva yense ndi zida
zonse zimene zimapezeka m'Nyumba ya Mulungu zimene ankazisamalira
Obedi-Edomu, pamodzinso ndi chuma cha m'nyumba yaufumu ndipo
anatenga anthu ngati chikole.

25 Amaziya mwana wa Yowasi mfumu ya Yuda anakhala ndi moyo
kwa zaka khumi ndi zisanu atamwalira Yehowasi mwana wa Yehowahazi
mfumu ya Israeli. 26 Ntchito zina za mfumu Amaziya, kuyambira
pachiyambi mpaka pa mapeto, kodi sizinalembedwe m'buku la mafumu
a Yuda ndi Israeli? 27 Kuyambira nthawi imene Amaziya analeka
kutsatira Yehova anthu anamukonzera chiwembu mu Yerusalemu ndipo
anathawira ku Lakisi, koma adaniwo anatumiza anthu ku Lakisiko

ndipo anamupha komweko. 28 Iwo anabwera naye ali pa kavalo ndipo
anayikidwa m'manda ndi makolo ake mu mzinda wa Yuda.

# 26

*Uziya Mfumu ya Yuda*

1 Kenaka anthu onse a ku Yuda anatenga Uziya amene anali wa zaka
16, namuyika kukhala mfumu m'malo mwa Amaziya abambo ake. 2 Iye
anamanganso mzinda wa Eloti ndi kuwubwezeranso ku Yuda abambo ake
atamwalira.
3 Uziya anali wa zaka 16 pamene anakhala mfumu ndipo analamulira
mu Yerusalemu kwa zaka 70. Dzina la amayi ake linali Yekoliya wa ku
Yerusalemu. 4 Iye anachita zolungama pamaso pa Yehova, monga momwe
anachitira Amaziya abambo ake. 5 Iye anapembedza Mulungu nthawi ya
Zekariya, amene ankamulangiza za kuopa Mulungu amene anamupatsa
chipambano.
6 Iyeyo anapita kukachita nkhondo ndi Afilisti ndipo anagwetsa makoma
a Gati, Yabine ndi Asidodi. Ndipo kenaka anamanganso mizinda ya
pafupi ndi Asidodi ndi malo ena pafupi ndi Afilisti. 7 Mulungu ana-
muthandiza polimbana ndi Afilisti ndi Aarabu amene amakhala ku Guri-
Baala ndiponso polimbana ndi Ameuni. 8 Aamoni ankabweretsa msonkho
kwa Uziya ndipo mbiri yake inamveka mpaka ku malire a dziko la Igupto
chifukwa anali wamphamvu kwambiri.
9 Uziya anamanga nsanja ku Yerusalemu ku Chipata Chapangodya, ku
Chigwa cha Chipata ndi pokhotera mpanda, ndipo anayikamo chitetezo.
10 Iye anamanganso nsanja ku chipululu ndi kukumbanso zitsime zambiri
chifukwa anali ndi ziweto zambiri m'mbali mwa phiri ndi ku zigwa.
Iye anali ndi anthu amene ankagwira ntchito m'minda yake ndiponso
m'minda yake ya mphesa m'phiri ndi malo achonde, pakuti ankakonda
nthaka.
11 Uziya anali ndi gulu lankhondo lophunzitsidwa bwino, lokonzekera
kupita ku nkhondo m'magulu monga mwa chiwerengero chawo chimene
mlembi Yeiyeli ndi Maaseya anasonkhanitsa motsogozedwa ndi Hananiya
mmodzi mwa akuluakulu a mfumu. 12 Chiwerengero chonse cha atsogoleri
a m'mabanja oyang'anira anthu ochita nkhondo chinali 2,600. 13 Pansi
pa ulamuliro wawo panali asilikali 307,500 ophunzitsidwa nkhondo,
gulu lamphamvu lothandiza mfumu kulimbana ndi adani ake. 14 Uziya
anawapangira asilikaliwo zishango, mikondo, zipewa zankhondo, malaya
ankhondo achitsulo, mauta ndi miyala yogendera. 15 Mu Yerusalemu
anapanga makina okonzedwa ndi anthu aluso amene amagwiritsidwa
ntchito pa malo otetezera a pa nsanja ndi pa ngodya kuponyera mivi ndi
kugubuduzira miyala. Mbiri yake inamveka kutali ndi ponseponse pakuti
anathandizidwa kwambiri mpaka anakhala wamphamvu kwambiri.
16 Koma pamene Uziya anakhala wamphamvu kwambiri, kunyada
kwake kunamuwononga. Iye sanakhulupirike kwa Yehova Mulungu
wake, ndipo analowa m'Nyumba ya Yehova kukafukiza lubani pa guwa
lofukizira. 17 Wansembe Azariya pamodzi ndi ansembe a Yehova ena
80 olimba mtima anamutsatira. 18 Iwo anatsutsana naye ndipo anati,
"Sibwino kuti inu mfumu muzifukiza lubani koma zidzukulu za Aaroni,
zimene zinapatulidwa kuti zizifukiza lubani. Chokani pa malo opatulika
ano, pakuti inu mwakhala osakhulupirika, ndipo simudzalemekezedwa
ndi Yehova Mulungu."

[19] Uziya, amene anali ndi chofukizira m'manja mwake wokonzeka
kuti afukize lubani, anapsa mtima. Iye anakwiyira ansembewo. Ndipo
ansembe aja akuona patsogolo pa guwa lofukizira lubani m'Nyumba
ya Mulungu, khate linayamba pamphumi pake. [20] Azariya, mkulu wa
ansembe pamodzi ndi ansembe ena onse atamuyang'ana anaona kuti
anali ndi khate pamphumi pake, ndipo anamutulutsa mofulumira. Ndipo
iye mwini anafulumira kutuluka, chifukwa Yehova anamulanga.
[21] Mfumu Uziya anali ndi khate mpaka tsiku limene anamwalira. Iye
amakhala m'nyumba ya yekha ngati wakhate, ndipo samalowa m'Nyumba
ya Yehova. Yotamu mwana wake ndiye amayang'anira nyumba yaufumu
ndipo ankalamulira anthu a m'dzikomo.
[22] Ntchito zina za mfumu Uziya, kuyambira pachiyambi mpaka pa
mapeto, zinalembedwa ndi mneneri Yesaya mwana wa Amozi. [23] Uziya
analondola makolo ake, ndipo anamuyika pamodzi ndi makolo ake ku
malo a manda a mafumu, koma osati m'manda mwawomo poti anthu
anati, "Iyeyu anali ndi khate." Ndipo Yotamu mwana wake analowa
ufumu m'malo mwake.

# 27

*Yotamu Mfumu ya Yuda*

[1] Yotamu anakhala mfumu ali ndi zaka 25 ndipo analamulira mu
Yerusalemu kwa zaka 16. Dzina la amayi ake linali Yerusa mwana wa
Zadoki. [2] Iye anachita zolungama pamaso pa Yehova, monga anachitira
Uziya abambo ake, kupatula kuti iyeyo sanalowe m'Nyumba ya Yehova.
Komabe anthu anapitirira kuchita zoyipa. [3] Yotamu anamanganso chipata
chakumtunda cha Nyumba ya Yehova ndipo anagwira ntchito yayikulu
yomanga khoma la ku phiri la Ofeli. [4] Iye anamanga mizinda m'mapiri
a ku Yuda ndipo anamanganso malinga ndi nsanja m'madera a ku
nkhalango.
[5] Yotamu anachita nkhondo ndi mfumu ya Aamoni ndipo anawag-
onjetsa. Chaka chimenecho Aamoni anapereka makilogalamu 3,400,
matani 1,000 a tirigu ndiponso matani 1,000 a barele. Aamoni anabw-
eretsa zinthu zomwezi chaka chachiwiri ndi chachitatu.
[6] Yotamu anakula mphamvu chifukwa anayenda molungama pamaso pa
Yehova Mulungu wake.
[7] Zina ndi zina zokhudza ulamuliro wa Yotamu, kuphatikizapo nkhondo
zake zonse ndi zinthu zina zimene anachita, zinalembedwa m'buku la
mafumu a Israeli ndi Yuda. [8] Iye anakhala mfumu ali ndi zaka 25 ndipo
analamulira mu Yerusalemu kwa zaka 16. [9] Yotamu anamwalira ndipo
anayikidwa m'manda mu Mzinda wa Davide. Ndipo Ahazi mwana wake
analowa ufumu m'malo mwake.

# 28

*Ahazi Mfumu ya Yuda*

[1] Ahazi anali ndi zaka makumi awiri pamene anakhala mfumu ndipo
analamulira mu Yerusalemu kwa zaka 16. Iye sanachite zolungama
pamaso pa Yehova, monga momwe anachitira Davide kholo lake. [2] Iye
anayenda m'njira za mafumu a Israeli ndipo anawumbanso mafano a
chipembedzo cha Abaala. [3] Iye amapsereza nsembe ku chigwa cha
Hinomu, ndipo anaperekanso ana ake aamuna ngati nsembe yopsereza
kutsatira njira zonyansa za mitundu imene Yehova anayithamangitsa

pamaso pa Aisraeli. 4 Iyeyo ankapereka nsembe ndi kufukiza lubani pa
malo opembedzerapo mafano, pamwamba pa mapiri ndi pansi pa mtengo
uliwonse waukulu.

5 N'chifukwa chake Yehova Mulungu wake anamupereka m'manja mwa
mfumu ya Aramu. Aaramu anamugonjetsa ndipo anagwira ukapolo anthu
ake ambiri napita nawo ku Damasiko.

Yehova anamuperekanso m'manja mwa mfumu ya Israeli, imene
inamuzunza ndi kumuphera anthu ake ambiri. 6 Pa tsiku limodzi, Peka
mwana wa Remaliya anapha asilikali 120,000 mu Yuda chifukwa Yuda
anasiya Yehova, Mulungu wa makolo awo. 7 Zikiri msilikali wa ku
Efereimu, anapha Maaseya mwana wa mfumu, Azirikamu woyang'anira
nyumba yaufumu, ndi Elikana wachiwiri kwa mfumu. 8 Aisraeli anagwira
ukapolo abale awo, akazi, ana aamuna ndi ana aakazi okwanira 200,000.
Iwo anafunkhanso katundu wambiri amene anapita naye ku Samariya.

9 Koma kumeneko kunali mneneri wa Yehova dzina lake Odedi,
ndipo anapita kukakumana ndi gulu lankhondo pamene linabwerera ku
Samariya. Iye anawawuza kuti, "Chifukwa Yehova, Mulungu wa makolo
anu anakwiyira Ayuda, Iye anawapereka m'dzanja lanu. Koma inu
mwawapha mwaukali, ukali wake wofika mpaka kumwamba. 10 Ndipo
tsopano mukufuna kuti amuna ndi akazi a ku Yuda ndi ku Yerusalemu
akhale akapolo anu. 11 Tsono mvereni! Abwezeni abale anu amene
mwawagwira ukapolo, pakuti mkwiyo wa Yehova uli pa inu."

12 Tsono atsogoleri ena a ku Efereimu, Azariya mwana wa Yehohanani,
Berekiya mwana wa Mesilemoti, Yehizikiya mwana wa Salumu, ndi Amasa
mwana wa Hadilayi anatsutsana nawo amene ankachokera ku nkhondo
kuja. 13 Iwo anati, "Musabweretse akapolowo kuno, pakuti ife tidzakhala
olakwa pamaso pa Yehova. Kodi mukufuna kuwonjezera pa machimo
athu ndi kulakwa kwathu? Pakuti zolakwa zathu ndi zambiri kale ndipo
mkwiyo wake woopsa uli pa Israeli."

14 Kotero asilikali aja anawasiya akapolowo pamodzi ndi katundu
amene analanda ku nkhondo pamaso pa akuluakulu ndi gulu lonse la
anthu. 15 Anthu amene atchulidwa mayina aja anatenga akapolowo,
ndipo kuchokera pa zolanda ku nkhondo, anawaveka onse amene anali
maliseche. Anawapatsa zovala ndi nsapato, chakudya ndi chakumwa ndi
mankhwala. Onse amene anali ofowoka anawakweza pa abulu. Choncho
anabwera nawo kwa abale awo ku Yeriko, Mzinda wa Migwalangwa,
ndipo kenaka anawabweza ku Samariya.

16 Pa nthawi imeneyo mfumu Ahazi inatumiza mawu kwa mfumu ya ku
Asiriya kupempha chithandizo. 17 Ankhondo a ku Edomu anabweranso
ndi kuthira nkhondo Yuda ndi kugwira akapolo. 18 Pamenepo n'kuti
Afilisti atathira nkhondo mizinda ya m'mbali mwa phiri ndi ku Negevi
ku Yuda. Iwo analanda mizindayo nakhala ku Beti-Semesi, Ayaloni ndi
Gederoti, komanso Soko, Timna ndi Gimizo pamodzi ndi midzi yawo
yozungulira. 19 Yehova anapeputsa Yuda chifukwa cha mfumu Ahazi
ya Israeli, pakuti analimbikitsa zoyipa ku Yuda ndipo anali munthu
wosakhulupirika kwambiri pamaso pa Yehova. 20 Tigilati-Pileseri mfumu
ya ku Asiriya anabwera kwa iye, ndipo anabweretsa mavuto m'malo
momuthandiza. 21 Ahazi anatenga zinthu zochokera m'Nyumba ya Yehova
ndi m'nyumba yaufumu ndi kwa atsogoleri ndipo anazipereka kwa
mfumu ya ku Asiriya, koma zimenezo sizinamuthandize.

22 Pa nthawi yake yamavutoyi mfumu Ahazi inapitirira kukhalabe
yosakhulupirika pamaso pa Yehova. 23 Ahazi ankapereka nsembe kwa
milungu ya ku Damasiko, imene inamugonjetsa. Iye ankaganiza kuti,
"Popeza milungu ya mafumu a Aaramu yawathandiza, ine ndidzapereka
nsembe kwa iyo kuti indithandize." Koma iyoyo inakhala kugwa kwake
ndi kugwa kwa Aisraeli onse.
24 Ahazi anasonkhanitsa pamodzi zinthu zonse kuchokera m'Nyumba
ya Mulungu ndipo anazitenga. Iye anatseka zitseko za Nyumba ya
Yehova ndipo anayimika maguwa ansembe pa ngodya iliyonse ya msewu
mu Yerusalemu. 25 Mu mzinda uliwonse wa Yuda anamangamo malo
achipembedzo, operekerapo nsembe zopsereza kwa milungu ina ndipo
anaputa mkwiyo wa Yehova, Mulungu wa makolo ake.
26 Zochitika zina pa ulamuliro wake ndi machitidwe ake onse, kuyam-
bira pachiyambi mpaka pa mapeto, zalembedwa m'buku la mafumu a
Yuda ndi Israeli. 27 Ahazi anamwalira ndipo anayikidwa mu mzinda
wa Yerusalemu, koma sanamuyike m'manda a mafumu a Israeli. Ndipo
Hezekiya mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

# 29

### *Mfumu Hezekiya Ayeretsa Nyumba ya Mulungu*

1 Hezekiya anali wa zaka 25 pamene anakhala mfumu ndipo anala-
mulira mu Yerusalemu kwa zaka 29. Dzina la amayi ake linali Abiya
mwana wa Zekariya. 2 Iye anachita zolungama pamaso pa Yehova, monga
momwe anachitira Davide abambo ake.
3 Pa chaka choyamba cha ulamuliro wake, iye anatsekula zitseko za
Nyumba ya Yehova ndipo anazikonza. 4 Iye analowetsamo ansembe
ndi Alevi ndipo anawasonkhanitsa ku bwalo lakummawa 5 ndipo anati:
"Mverani, inu Alevi! Dziyeretseni tsopano ndiponso muyeretse Nyumba
ya Yehova Mulungu wa makolo anu. Muchotse zodetsa zonse ku malo
opatulika. 6 Makolo athu anali osakhulupirika ndipo anachita zoyipa pa
maso pa Yehova Mulungu wathu ndi kumusiya Yehovayo. Iwo anatem-
benuka ndi kusiya malo okhalako Yehova ndi kumufulatira. 7 Iwowo
anatsekanso zitseko zapakhonde ndi kuzimitsa nyale. Sanafukize lubani
kapena kupereka nsembe zopsereza ku malo opatulika a Mulungu wa
Israeli. 8 Kotero, Yehova anakwiyira Yuda ndi Yerusalemu. Iye anawasan-
dutsa chinthu chochititsa mantha, choopsa ndiponso chonyozedwa monga
momwe mukuonera ndi maso anuwa lero lino. 9 Ichi n'chifukwa chake
makolo athu anaperekedwa ku lupanga ndipo n'chifukwa chake ana
athu aamuna ndi aakazi ndi akazi athu ali ku ukapolo. 10 Tsono ine
ndikuganiza zochita pangano ndi Yehova Mulungu wa Israeli, kuti mkwiyo
wake woopsawu utichokere. 11 Ana anga, musanyalanyaze tsopano, pakuti
Yehova wakusankhani kuti muziyima pamaso pake ndi kumutumikira Iye,
kugwira ntchito pamaso pake ndi kufukiza lubani."
12 Ndipo Alevi awa anakonzeka kugwira ntchito:
Kuchokera ku banja la Kohati,
Mahati mwana wa Amasai ndi Yoweli mwana wa Azariya;
kuchokera ku banja la Merari,
Kisi mwana wa Abidi ndi Azariya mwana wa Yehaleleli;
kuchokera ku banja la Geresoni,
Yowa mwana wa Zima ndi Edeni mwana wa Yowa;
13 kuchokera kwa zidzukulu za Elizafani,

Simiri ndi Yeiyeli;
kuchokera kwa zidzukulu za Asafu,
Zekariya ndi Mataniya;
14 kuchokera kwa zidzukulu za Hemani,
Yehieli ndi Simei;
kuchokera kwa zidzukulu za Yedutuni,
Semaya ndi Uzieli.

15 Atasonkhanitsa abale awo ndi kudziyeretsa, iwo anapita kukayeretsa
Nyumba ya Yehova, monga inalamulira mfumu, potsatira mawu a
Yehova. 16 Ansembe analowa ku malo opatulika a Yehova kukayeretsako.
Anatulutsira ku bwalo la Nyumba ya Yehova chilichonse chodetsedwa
chimene anachipeza m'Nyumba ya Yehova. Alevi anatenga zimenezo
ndi kupita nazo ku chigwa cha Kidroni. 17 Iwo anayamba mwambo
woyeretsawu tsiku loyamba la mwezi woyamba ndipo pa tsiku lachisanu
ndi chitatu la mweziwo anafika pa khonde la nyumba ya Yehova. Tsono
anachita mwambo woyeretsa Nyumba ya Yehova ija masiku asanu ndi
atatu, ndipo anamaliza pa tsiku la 16 mwezi woyamba.

18 Ndipo anapita kwa mfumu Hezekiya ndi kukafotokoza kuti, "Ife
tayeretsa Nyumba ya Mulungu yonse, guwa lansembe zopsereza ndi
ziwiya zake zonse, ndiponso tebulo limene timayikapo buledi wopatulika
pamodzi ndi zinthu zake zonse. 19 Takonza ndi kuyeretsa zinthu zonse
zimene mfumu Ahazi anazichotsa mwa kusakhulupirika kwake pamene
anali mfumu. Taziyika kutsogolo kwa guwa la Yehova."

20 Mmamawa tsiku linalo, mfumu Hezekiya inasonkhanitsa pamodzi
akuluakulu a mu mzindawo ndipo inapita ku Nyumba ya Yehova.
21 Iwo anabweretsa ng'ombe zazimuna zisanu ndi ziwiri ndi nkhosa
zazimuna zisanu ndi ziwiri, ana ankhosa aamuna asanu ndi awiri, mbuzi
zazimuna zisanu ndi ziwiri monga nsembe zoperekedwa chifukwa cha
tchimo la ufumu, la malo opatulika ndi Yuda. Tsono mfumu inalamula
ansembe, zidzukulu za Aaroni, kuti apereke zimenezi pa guwa lansembe la
Yehova. 22 Choncho anthuwo anapha ng'ombe zazimunazo ndipo ansembe
anatenga magazi ake ndi kuwawaza pa guwa lansembe, kenaka anapha
nkhosa zazimuna zija ndipo anawaza magazi ake pa guwa lansembe;
anaphanso ana ankhosa aja ndipo anawaza magazi ake pa guwa lansembe.
23 Mbuzi zoperekedwa chifukwa cha tchimo zija zinabweretsedwa pamaso
pa mfumu ndi anthu onse, ndipo anasanjika manja awo pa izo. 24 Kenaka
ansembe anapha mbuzizo ndipo anapereka magazi ake pa guwa, kuti
ukhale mwambo wofafanizira machimo a Aisraeli onse, pakuti mfumu
inalamula kuti nsembe yopsereza ndi yopepesera machimo zichitike
chifukwa cha Aisraeli onse.

25 Iye anayika Alevi m'Nyumba ya Yehova ali ndi ziwaya za malipenga,
azeze ndi apangwe potsata lamulo la Davide, Gadi mlosi wa mfumu ndi
mneneri Natani. Pakuti Yehova ndiye analamula zimenezi kudzera mwa
aneneri. 26 Kotero Alevi anayima okonzekera atanyamula zoyimbira za
Davide ndiponso ansembe atanyamula malipenga awo.

27 Hezekiya analamulira kuti apereke nsembe zopsereza pa guwa.
Pamene amayamba kupereka nsembezo, kuyimbira Yehova kunayam-
bikanso, pamodzi ndi malipenga ndi zipangizo zoyimbira za Davide
mfumu ya Israeli. 28 Anthu onse anawerama pansi ndi kulambira, pamene
oyimba amayimba ndi malipenga. Izi zonse zinapitirira mpaka pa mapeto
pa nsembe zopsereza.

29 Zopereka zitatha, mfumu ndi wina aliyense amene anali naye
anagwada pansi ndi kulambira. 30 Mfumu Hezekiya ndi akuluakulu ake
analamulira Alevi kuti atamande Yehova potsata mawu a Davide ndi
mlosi Asafu. Kotero anayimba nyimbo zamatamando mokondwera ndipo
anaweramitsa mitu yawo ndi kulambira.

31 Kenaka Hezekiya anati, "Inu mwadzipereka tsopano kwa Yehova.
Bwerani ndipo mufike ndi nsembe ndi zopereka zachiyamiko ku Nyumba
ya Yehova." Choncho anthu onse anabweretsa nsembe ndi zopereka
zachiyamiko, ndipo anthu onse amene anali ofuna mu mtima mwawo
anabweretsa nsembe zopsereza.

32 Chiwerengero cha nsembe zopsereza chimene anthu onse anab-
weretsa chinali ng'ombe zazimuna makumi asanu ndi awiri, nkhosa
zazimuna 100, ana ankhosa aamuna 200 ndipo zonsezi zinali za nsembe
yopsereza kwa Yehova. 33 Ziweto zimene zinapatulidwa kukhala nsembe
zinalipo ng'ombe zazimuna 600, nkhosa ndi mbuzi 3,000. 34 Koma
ansembe anali ochepa kuti asende zonse zopsereza. Choncho abale awo
Alevi anawathandiza mpaka ntchito yonse inatha ndipo mpaka ansembe
ena atadziyeretsa, pakuti Alevi anachita changu kudziyeretsa kulekana
ndi momwe anachitira ansembe. 35 Panali nsembe zopsereza zochuluka,
pamodzi ndi mafuta a nsembe yachiyanjano ndi nsembe yachakumwa
imene imachitika pamodzi ndi nsembe yopsereza.

Kotero ntchito ya m'Nyumba ya Mulungu inakhazikitsidwanso.
36 Hezekiya ndi anthu onse anakondwera pa zimene Mulungu anachitira
anthu ake, chifukwa zinachita mwamsangamsanga.

# 30

### *Hezekiya Achita Chikondwerero cha Paska*

1 Hezekiya anatumiza uthenga m'dziko lonse la Israeli ndi ku Yuda
ndiponso analemba makalata ku Efereimu ndi Manase, oyitana anthu
kuti abwere ku Nyumba ya Yehova ku Yerusalemu kudzakondwerera
Paska wa Yehova, Mulungu wa Israeli. 2 Mfumu ndi akuluakulu ake
pamodzi ndi anthu onse a mu Yerusalemu anagwirizana kuti akondwerere
Paska pa mwezi wachiwiri. 3 Iwo sanathe kukondwerera pa nthawi yake
chifukwa si ansembe ambiri amene anadziyeretsa ndiponso anthu anali
asanasonkhane mu Yerusalemu. 4 Chikonzerochi chinaoneka kuti chinali
chabwino kwa mfumu pamodzi ndi anthu onse. 5 Iwo anagwirizana
zoti alengeze mu Israeli monse kuyambira ku Beeriseba mpaka ku
Dani, kuyitana anthu kuti abwere ku Yerusalemu ndi kudzakondwerera
Paska wa Yehova, Mulungu wa Israeli. Si ambiri amene ankachita
chikondwererochi monga momwe kunalembedwera.

6 Molamulidwa ndi mfumu, amithenga anapita mu Israeli yense ndi
Yuda ndi makalata ochokera kwa mfumu ndi kwa akuluakulu ake,
olembedwa kuti,

"Aisraeli bwererani kwa Yehova, Mulungu wa Abrahamu, Isake ndi
Israeli, kuti abwerere kwa inu amene mwatsala, amene mwapulumuka
m'dzanja la mafumu a ku Asiriya. 7 Musakhale ngati makolo anu ndi
abale anu, amene anali osakhulupirika kwa Yehova Mulungu wa makolo
awo kotero kuti anawachititsa kuti akhale chinthu chochititsa mantha,
monga mukuoneramu. 8 Musawumitse khosi monga anachitira makolo
anu, Gonjerani Yehova. Bwerani ku malo opatulika, amene anawapatula
kwamuyaya. Tumikirani Yehova Mulungu wanu kuti mkwiyo wake

ukuchokereni. 9 Ngati inu mubwerera kwa Yehova, pamenepo abale anu
ndi ana anu adzachitiridwa chifundo ndi amene anawagwira ukapolo
ndipo adzabwereranso ku dziko lino pakuti Yehova, Mulungu wanu
ndi wokoma mtima ndi wachifundo. Iye sadzakufulatirani ngati inuyo
mubwerera kwa Iye."

10 Amithenga aja anapita mzinda ndi mzinda wa ku Efereimu ndi
Manase mpaka ku Zebuloni, koma anthu anawanyoza ndi kuwachita
chipongwe. 11 Komabe anthu ena a ku Aseri, Manase ndi Zebuloni
anadzichepetsa ndipo anapita ku Yerusalemu. 12 Dzanja la Mulungu
linalinso pa anthu a ku Yuda, kuwapatsa mtima umodzi wochita zimene
mfumu ndi akuluakulu ake analamula potsata mawu a Yehova.

13 Gulu lalikulu la anthu linasonkhana mu Yerusalemu kudza-
chita chikondwerero cha Buledi Wopanda Yisiti pa mwezi wachi-
wiri. 14 Anachotsa mu Yerusalemu maguwa ofukizira lubani ndipo
anakawaponya m'chigwa cha Kidroni.

15 Iwo anapha mwana wankhosa wa Paska pa tsiku la 14 la mwezi
wachiwiri. Ansembe ndi Alevi anachita manyazi ndipo anadziyeretsa ndi
kubweretsa nsembe zopsereza ku Nyumba ya Yehova. 16 Ndipo anakhala
m'malo awo a nthawi zonse potsatira zolembedwa m'malamulo a Mose
munthu wa Mulungu. Ansembe anawaza magazi amene anawapatsa
Alevi. 17 Popeza ambiri m'gululo anali asanadziyeretse, Alevi anapha
ana ankhosa a Paska a iwo amene, mwa mwambo, anali osayeretsedwa
ndipo sakanatha kupereka ana ankhosa awo kwa Yehova. 18 Ngakhale kuti
ambiri mwa anthu ochokera ku Efereimu, Manase, Isakara ndi Zebuloni
sanadziyeretse okha, komabe anadya Paska motsutsana ndi zimene
zinalembedwa. Koma Hezekiya anawapempherera, kunena kuti, "Yehova
wabwino, khululukirani aliyense 19 amene wayika mtima wake kufu-
nafuna Yehova, Mulungu wa makolo ake, ngakhale ali wosayeretsedwa
molingana ndi malamulo a malo opatulika." 20 Ndipo Yehova anamvera
Hezekiya ndipo anachiritsa anthuwo.

21 Aisraeli amene anali mu Yerusalemu anachita chikondwerero cha
Buledi Wopanda Yisiti kwa masiku asanu ndi awiri akusangalala
kwambiri, pamene Alevi ndi ansembe amayimbira Yehova tsiku lililonse,
akuyimbira zida zamatamando za Yehova.

22 Hezekiya anayankhula molimbikitsa Alevi onse amene anaonetsa
kumvetsa bwino za kutumikira Yehova. Kwa masiku asanu ndi awiri
anadya gawo lawo ndi kupereka nsembe zachiyanjano ndi kutamanda
Yehova, Mulungu wa makolo awo.

23 Ndipo msonkhano wonse unagwirizana zopitiriza chikondwerero
kwa masiku ena asanu ndi awiri. Kotero kwa masiku ena asanu ndi
awiri anachita chikondwererocho mosangalala. 24 Hezekiya mfumu ya
Yuda anapereka ng'ombe zamphongo 1,000 ndi nkhosa ndi mbuzi 7,000
ku msonkhanoko ndipo akuluakulu ake anapereka ng'ombe zamphongo
1,000, nkhosa ndi mbuzi 10,000. Ansembe ambiri anadziyeretsa. 25 Gulu
lonse la ku Yuda linasangalala, pamodzi ndi ansembe ndi Alevi ndi
onse amene anasonkhana ochokera ku Israeli, kuphatikizanso alendo
amene anachokera ku Israeli ndi amene amakhala ku Yuda. 26 Munali
chikondwerero chachikulu mu Yerusalemu, pakuti kuyambira masiku a
Solomoni mwana wa Davide mfumu ya Israeli sizinachitikepo zotere mu
Yerusalemu. 27 Ansembe ndi Alevi anayimirira kudalitsa anthu, ndipo

Mulungu anawamvera pakuti pemphero lawo linafika kumwamba, malo
ake oyera.

# 31

1 Zonse zitatha, Aisraeli onse amene anali kumeneko anapita ku mizinda
ya ku Yuda, nakaphwanya miyala yachipembedzo ndi kudula mitengo ya
mafano a Asera. Iwo anakawononga malo achipembedzo ndi maguwa
ansembe amene anali m'dziko lonse la Yuda, Benjamini, Efereimu ndi
Manase. Atawononga zonsezi, Aisraeli anabwerera ku mizinda yawo ndi
ku malo awo.

*Zopereka ku Ntchito ya Chipembedzo*

2 Hezekiya anakhazikitsa magulu a ansembe ndi Alevi, gulu lililonse
monga mwa ntchito zawo ngati ansembe kapena Alevi, kupereka nsembe
zopsereza ndi nsembe zachiyanjano, kutumikira, kuyamikira ndi kuyimba
matamando pa zipata za ku malo okhala Yehova. 3 Kuchokera pa
chuma chake, mfumu inapereka nsembe zopsereza za mmawa ndi
madzulo ndiponso nsembe zopsereza za pa Chikondwerero cha Masabata,
Chikondwerero cha Mwezi Watsopano ndipo inakhazikitsa zikondwerero
monga zinalembedwera m'malamulo a Yehova. 4 Iyo inalamula anthu
amene amakhala mu Yerusalemu kupereka gawo lawo kwa ansembe
ndi Alevi kuti iwowo adzipereke ku malamulo a Yehova. 5 Lamuloli
atangolilengeza, Aisraeli anapereka mowolowamanja zipatso zoyamba
kucha za tirigu, vinyo watsopano, mafuta ndi uchi ndi zonse zomwe
nthaka yawo inabereka. Anabweretsa zochuluka kwambiri, chakhumi
cha chilichonse. 6 Aisraeli ndi Ayuda amene amakhala m'mizinda ya Yuda
anabweretsanso chakhumi cha ng'ombe zawo ndi nkhosa ndi chakhumi
cha zinthu zoyera zoperekedwa kwa Yehova Mulungu wawo, ndipo
anaziyika m'milumilu. 7 Anayamba kuchita izi mwezi wachitatu ndipo
anatsiriza mwezi wachisanu ndi chiwiri. 8 Hezekiya ndi akuluakulu ake
atabwera ndi kuona miluyo, anatamanda Yehova ndi kudalitsa anthu ake,
Aisraeli.

9 Hezekiya anafunsa ansembe ndi Alevi za miluyi; 10 ndipo Azariya,
mkulu wa ansembe, ochokera ku banja la Zadoki anayankha kuti,
"Kuyambira pamene anthu anayamba kubweretsa zopereka zawo ku
Nyumba ya Yehova ife takhala ndi zokwanira kudya ndi zina zambiri
zosunga, chifukwa Yehova wadalitsa anthu ake, ndipo mulu umenewu
ndiye zotsala."

11 Hezekiya analamula kuti akonze zipinda zosungiramo za m'Nyumba
ya Yehova, ndipo izi zinachitika. 12 Ndipo iwo mokhulupirika anabweretsa
zopereka, chakhumi ndi mphatso zopatulika. Konaniya Mlevi ndiye
amayang'anira zinthu zimenezi ndipo m'bale wake Simei ndiye anali
wachiwiri wake. 13 Yehieli, Azaziya, Nahati, Asaheli, Yerimoti, Yozabadi,
Elieli, Isimakiya, Mahati ndi Benaya anali oyang'anira motsogozedwa ndi
Konaniya ndi Simei, m'bale wake. Iwowa anasankhidwa ndi mfumu
Hezekiya ndi Azariya mkulu woyang'anira Nyumba ya Mulungu.

14 Kore mwana wa Imuna Mlevi, mlonda wa Chipata Chakummawa,
amayang'anira zopereka zaufulu kwa Mulungu, ankagawa zopereka za
kwa Yehova ndiponso mphatso zopatulika. 15 Edeni, Miniyamini, Yesuwa,
Semaya, Amariya, Sekaniya amamuthandiza mokhulupirika m'mizinda
yonse a ansembe kugawira kwa ansembe anzawo monga mwa magulu
awo, aakulu ndi aang'ono omwe.

[16] Kuwonjezera apa, amagawira ana aamuna a zaka zitatu kapena
kupitirira amene mayina awo anali m'mbiri ya mibado yawo, amene
adzalowe m'Nyumba ya Yehova kugwira ntchito za tsiku ndi tsiku za
magulu awo, molingana ndi udindo ndi magulu awo. [17] Ndipo anazigawa
kwa ansembe amene analembetsa mayina awo mwa mbiri ya mabanja
awo, chimodzimodzinso Alevi amene anali ndi zaka makumi awiri
kapena kupitirira molingana ndi udindo wawo ndi magulu awo. [18] Iwo
anaphatikizanso ana onse aang'ono, akazi ndiponso ana aamuna ndi ana
aakazi a gulu lonse amene analembedwa m'mbiri ya mibado yawo iyi,
pakuti anakhulupirika pa kudzipatula okha.

[19] Kunena za ansembe, zidzukulu za Aaroni, amene amakhala
m'minda yozungulira mizinda yawo kapena mzinda wina uliwonse,
anthu anasankhidwa mowatchula mayina kuti azipereka magawo kwa
munthu wamwamuna aliyense pakati pawo ndiponso kwa onse amene
analembedwa m'mbiri ya mibado ya Alevi.

[20] Izi ndi zimene Hezekiya anachita mu Yuda monse, kuchita zabwino,
zolungama ndi zokhulupirika pamaso pa Yehova Mulungu wake. [21] Pa
chilichonse chimene anachita pa ntchito ya Nyumba ya Mulungu ndi pa
kumvera malangizo ndi malamulo, iye anafunafuna Mulungu wake ndipo
anagwira ntchito ndi mtima wake wonse. Ndipo zinthu zimamuyendera
bwino.

# 32

*Senakeribu Aopseza Yerusalemu*

[1] Zitatha zonse zimene Hezekiya anachita mokhulupirika, Senakeribu
mfumu ya ku Asiriya anabwera ndi kuthira nkhondo dziko la Yuda.
Iye anazinga mizinda yotetezedwa ya Yuda, kuganiza kuti ayigonjetsa.
[2] Pamene Hezekiya anaona kuti Senakeribu wabwera ndipo wakonzeka
kuchita nkhondo ndi Yerusalemu, [3] iye anakambirana ndi akuluakulu ake
pamodzi ndi atsogoleri a gulu lankhondo za kutseka akasupe ochoka ku
kasupe amene anali kunja kwa mzinda, ndipo iwo anamuthandiza. [4] Gulu
lalikulu la anthu linasonkhana, ndipo anatseka akasupe onse pamodzi ndi
mtsinje umene umayenda m'kati mwa nthakamo. Iwo ankanena kuti,
"N'chifukwa chiyani mafumu a Asiriya akabwera kuno adzapeze madzi
ambiri?" [5] Kenaka iye anagwira ntchito molimbika kukonza madera
ogumuka a khoma ndi kumangapo msanja. Anamanganso mpanda wina
kunja kwa mpanda winawo ndipo anamanga zolimbitsa Milo ku mzinda
wa Davide.

[6] Iye anasankha atsogoleri a ankhondo olamulira anthu ndipo anawa-
sonkhanitsa pamaso pake pa bwalo la chipata cha mzinda ndi kuwalimbik-
itsa ndi mawu awa: [7] "Khalani amphamvu ndi olimba mtima. Musachite
mantha kapena kutaya mtima chifukwa cha mfumu ya ku Asiriya ndi gulu
lalikulu lankhondo limene ali nalo, pakuti ife tili ndi mphamvu yayikulu
kuposa imene ili ndi iye. [8] Iye ali ndi mphamvu ya anthu basi, koma ife
tili ndi Yehova Mulungu wathu kutithandiza ndi kuchita nkhondo zathu."
Ndipo anthu anapeza chilimbikitso kuchokera pa zimene Hezekiya mfumu
ya Yuda ananena.

[9] Nthawi ina, pamene Senakeribu mfumu ya ku Asiriya ndi gulu lake
lonse lankhondo anali atazinga Lakisi, iye anatumiza atsogoleri ake
ankhondo ku Yerusalemu ndi uthenga uwu kwa Hezekiya mfumu ya Yuda
ndi anthu onse a ku Yuda amene anali kumeneko:

10 “Senakeribu mfumu ya ku Asiriya akuti: Kodi inu mukukhulupirira
chiyani, kuti mukukhalabe mu Yerusalemu mutazingidwa? 11 Pamene
Hezekiya akunena kuti ‘Yehova Mulungu wathu adzatipulumutsa ku-
choka m’dzanja la mfumu ya ku Asiriya,’ iye akukusocheretsani, kuti
mufe ndi njala ndi ludzu. 12 Kodi si Hezekiya amene anachotsa malo
opembedzerapo Mulungu ameneyu ndi maguwa ansembe ndi kunena
kwa anthu a ku Yuda ndi Yerusalemu kuti, ‘Muzipembedza pa guwa
lansembe limodzi ndi kupserezapo nsembe?’

13 “Kodi inu simukudziwa zimene ine ndi makolo anga tachita kwa
anthu a mitundu ina? Kodi milungu ya mitundu imeneyi inatha
kupulumutsa dziko lawo kuchoka m’dzanja langa? 14 Kodi ndi milungu
iti mwa milungu ya mitundu ina ya anthuwo, imene makolo anga
anayiwononga kotheratu, inatha kupulumutsa anthu ake m’dzanja
langa? Nanga tsono Mulungu wanuyo adzakupulumutsani m’dzanja
langa motani? 15 Choncho inu musalole kuti Hezekiya akunamizeni
ndi kukusocheretsani motere. Musamukhulupirire, pakuti palibe
mulungu wa mtundu wina uliwonse kapena ufumu wina uliwonse
umene unatha kupulumutsa anthu ake kuchoka m’dzanja langa kapena
m’dzanja la makolo anga. Nanga bwanji Mulungu wanuyo, sadzatha
kukupulumutsani kuchoka m’dzanja langa!”

16 Atsogoleri a ankhondo a Senakeribu anapitiriza kuyankhula zotsut-
sana ndi Yehova Mulungu ndi mtumiki wake Hezekiya. 17 Mfumunso
inalemba makalata onyoza Yehova, Mulungu wa Israeli, ndipo inanena
zotsutsana naye izi: “Monga momwe milungu ya anthu a mayiko ena
sinathe kuwapulumutsa kuchoka m’dzanja langa, chonchonso Mulungu
wa Hezekiya sadzapulumutsa anthu ake kuchoka m’dzanja langa.”
18 Kenaka iwo anafuwula mu Chihebri kwa anthu a mu Yerusalemu amene
anali pa khoma, kuwaopseza ndi kuwachititsa mantha ndi cholinga choti
alande mzindawo. 19 Iwo anayankhula za Mulungu wa Yerusalemu monga
anayankhulira za milungu ya anthu ena a pa dziko lapansi, ntchito ya
manja a anthu.

20 Mfumu Hezekiya ndi mneneri Yesaya mwana wa Amozi anafuwulira
kumwamba m’pemphero chifukwa cha zimenezi. 21 Ndipo Yehova
anatumiza mngelo amene anadzapha anthu onse odziwa nkhondo ndi
atsogoleri ndiponso oyang’anira misasa ya mfumu ya ku Asiriya. Choncho
Senakeribu anabwerera kwawo wamanyazi. Ndipo atalowa m’nyumba ya
mulungu wake, ena mwa ana ake anamupha ndi lupanga.

22 Kotero Yehova anapulumutsa Hezekiya ndi anthu a ku Yerusalemu
kuchoka m’dzanja la Senakeribu mfumu ya ku Asiriya ndi m’dzanja
la anthu ena. Yehova anawateteza ku mbali zonse. 23 Anthu ambiri
anabweretsa zopereka kwa Yehova ku Yerusalemu ndi mphatso zamten-
gowapatali kwa Hezekiya mfumu ya Yuda. Kuyambira nthawi imeneyo
Hezekiya ankalemekezedwa kwambiri ndi mitundu ina yonse.

### *Kunyada, Kupambana ndi Imfa ya Hezekiya*

24 Pa nthawi imeneyo Hezekiya anadwala ndipo anali pafupi kufa.
Iye anapemphera kwa Yehova, amene anamuyankha ndi kumupatsa
chizindikiro chodabwitsa. 25 Koma Hezekiya anali ndi mtima wonyada
ndipo sanachite molingana ndi kukoma mtima kumene Mulungu ana-
muonetsera. Choncho mkwiyo wa Yehova unali pa iye ndi pa Yuda ndi
Yerusalemu. 26 Koma kenaka Hezekiya analapa za kunyada kwakeko,

monga anachitanso anthu a mu Yerusalemu. Choncho mkwiyo wa Yehova sunafike pa iwo pa nthawi ya Hezekiya.

27 Hezekiya anali ndi chuma ndi ulemu wambiri ndipo anamanga
nyumba zosungiramo chuma cha siliva wake ndi golide ndi za miyala
yokongola, zokometsera zakudya, zishango ndi mtundu uliwonse wa
zinthu zamtengowapatali. 28 Iye anamanganso nyumba zosungiramo
tirigu, vinyo watsopano ndi mafuta a olivi, ndiponso anamanga nyumba
zodyeramo ng'ombe zosiyanasiyana, ndi makola a nkhosa. 29 Iyeyo
anamanga midzi ndipo anali ndi nkhosa ndi ng'ombe zambiri, pakuti
Mulungu anamupatsa chuma chambiri.

30 Ndi Hezekiya amene anatseka ku mtunda kwa kasupe wa Gihoni,
ndi kumuwongolera kuti madzi ake apite mbali ya kumadzulo kwa
Mzinda wa Davide. Iye ankachita bwino pa ntchito iliyonse imene
ankagwira. 31 Koma pamene nthumwi zotumizidwa ndi atsogoleri a ku
Babuloni zinabwera kudzamufunsa za chizindikiro chozizwitsa chimene
chinachitika m'dzikomo, Mulungu anamusiya yekha, kumuyesa kuti
adziwe zonse zimene zinali mu mtima mwake.

32 Zina ndi zina zokhudza ulamuliro wa Hezekiya ndi ntchito za
kudzipereka kwake zalembedwa m'masomphenya a Yesaya mwana wa
Amozi, m'buku la mafumu a Yuda ndi Israeli. 33 Hezekiya anamwalira
ndipo anayikidwa m'manda pa phiri pamene pali manda a zidzukulu
za Davide. Ayuda onse ndi anthu a mu Yerusalemu anamulemekeza
atamwalira. Ndipo Manase mwana wake analowa ufumu m'malo mwake.

# 33

*Manase Mfumu ya Yuda*

1 Manase anali wa zaka khumi ndi ziwiri pamene anakhala mfumu,
ndipo analamulira mu Yerusalemu kwa zaka 55. 2 Iye anachita zoyipa
pamaso pa Yehova, potsatira machitidwe a mitundu imene Yehova
anayithamangitsa pamaso pa Aisraeli. 3 Iyeyo anamanganso malo
opembedzerapo mafano amene Hezekiya abambo ake anawaphwasula;
anamanganso maguwa ansembe a Baala ndi kupanga mafano a Asera.
Iye amagwadira zolengedwa zonse zamlengalenga ndi kumazipem-
bedza. 4 Manase anamanga maguwa m'Nyumba ya Yehova, m'mene
Yehova ananena kuti, "Ine ndidzakhala mu Yerusalemu mpaka muyaya."
5 M'mabwalo onse awiri a Nyumba ya Yehova anamangamo maguwa
ansembe a zolengedwa zonse zamlengalenga. 6 Iye ankakapereka ana
ake aamuna ngati nsembe yopsereza ku chigwa cha Hinomu, ankachita
zamatsenga, kuwombeza ndi ufiti, ankakafunsira kwa woyankhula ndi
mizimu ya anthu akufa. Iye anachita zoyipa zambiri pamaso pa Yehova,
kumukwiyitsa Iyeyo.

7 Manase anatenga fano losema limene anapanga ndi kuliyika
m'Nyumba ya Mulungu, zimene Mulungu ananena kwa Davide ndi
kwa mwana wake Solomoni kuti, "M'nyumba ya Mulungu muno, mu
Yerusalemu muno, malo amene ndawasankha pakati pa mafuko onse a
Israeli, ndidzakhalamo mpaka muyaya. 8 Ine sindidzachotsanso phazi
la Aisraeli kuchoka m'dziko limene ndawapatsa makolo ako, ngatitu
iwowa adzasamalira kuchita chilichonse chimene ndinawalamulira za
malamulo onse, malangizo ndi miyambo imene inapatsidwa kudzera
mwa Mose." 9 Koma Manase anasocheretsa anthu a ku Yuda ndi

Yerusalemu, kotero anachita zoyipa zambiri kupambana mitundu imene Yehova anayiwononga pamaso pa Aisraeli.

10 Yehova anayankhula kwa Manase ndi anthu ake, koma iwo
sanasamaleko. 11 Kotero Yehova anawatumizira atsogoleri a ankhondo
a ku Asiriya amene anagwira Manase ukapolo, anayika ngowe m'mphuno
mwake, namumanga ndi zingwe zamkuwa ndi kupita naye ku Bab-
uloni. 12 Ali pa mavuto akewo anafunafuna kuti Yehova Mulungu
wake amukomere mtima ndipo anadzichepetsa kwakukulu pamaso pa
Mulungu wa makolo ake. 13 Ndipo atapemphera, Yehova anakhudzidwa
ndi kupempha kwakeko ndipo anamvera madandawulo ake. Kotero
anamubweretsanso ku Yerusalemu ndi ku ufumu wake. Ndipo Manase
anadziwa kuti Yehova ndi Mulungu.

14 Zitapita izi iye anamanga khoma la kunja kwa Mzinda wa Davide kumadzulo kwa kasupe wa Gihoni ku chigwa mpaka polowera ku Chipata cha Nsomba kuzungulira phiri la Ofeli. Iyeyo anakweza kwambiri khomalo. Anayikanso atsogoleri a nkhondo ku mizinda yonse yotetezedwa ya Yuda.

15 Iye anachotsa milungu yonse yachilendo ndi fano m'Nyumba ya
Yehova komanso maguwa ansembe onse amene anamanga pa phiri
la Nyumba ya Mulungu ndi mu Yerusalemu, nazitayira kunja kwa
mzinda. 16 Kenaka anabwezeretsa guwa lansembe la Yehova ndi kupereka
zopereka zachiyanjano ndiponso zopereka zamatamando ndipo anawuza
Yuda kuti atumikire Yehova Mulungu wa Israeli. 17 Komabe anthu
anapitiriza kupereka nsembe ku malo achipembedzo, koma kwa Yehova,
Mulungu wawo yekha.

18 Zina ndi zina zokhudza ulamuliro wa Manase, kuphatikiza mapem-
phero ake kwa Mulungu wake ndi mawu amene alosi anayankhula kwa
iye m'dzina la Yehova Mulungu wa Israeli, zalembedwa m'mabuku a
mafumu a Israeli. 19 Pemphero lake ndi momwe Mulungu anakhudzid-
wira ndi kupempha kwakeko, pamodzinso ndi machimo ake onse ndi
kusakhulupirika kwake, ndiponso malo onse amene anamanga, malo
azipembedzo ndi mafano a Asera ndi mafano asanadzichepetse, zonse
zalembedwa m'mbiri ya alosi. 20 Manase anamwalira ndipo anayikidwa
m'manda m'nyumba yake yaufumu. Ndipo Amoni mwana wake analowa
ufumu m'malo mwake.

### *Amoni Mfumu ya Yuda*

21 Amoni anali wa zaka 22 pamene anakhala mfumu ndipo analamulira
mu Yerusalemu kwa zaka ziwiri. 22 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova,
monga anachitira Manase abambo ake. Amoni analambira ndi kupereka
nsembe kwa mafano onse amene anapanga Manase. 23 Koma kusiyana
ndi abambo ake Manase, iye sanadzichepetse pamaso pa Yehova. Amoni
anawonjeza kulakwa kwake.

24 Akuluakulu a Amoni anamuchita chiwembu ndipo anamupha
m'nyumba yake yaufumu. 25 Koma anthu a m'dzikomo anapha onse
amene anakonzera chiwembu mfumu Amoni, ndipo anayika mwana wake
Yosiya kukhala mfumu m'malo mwake.

## 34

### *Yosiya Akonzanso Chipembedzo*

[1] Yosiya anali wa zaka zisanu ndi zitatu pamene anakhala mfumu, ndipo
analamulira mu Yerusalemu kwa zaka 31. [2] Iye anachita zolungama
pamaso pa Yehova ndi kutsata makhalidwe a Davide abambo ake,
osatembenukira kumanja kapena kumanzere.

[3] M'chaka chachisanu ndi chitatu cha ulamuliro wake, iye akanal-
ibe wamng'ono, anayamba kufunafuna Mulungu wa Davide abambo
ake. M'chaka cha khumi ndi chiwiri iye anayamba kuyeretsa Yuda
ndi Yerusalemu kuchotsa malo azipembedzo, mafano a Asera, milungu
yosema ndi mafano owumbidwa. [4] Maguwa ansembe a Baala anag-
wetsedwa iye atalamulira. Anadula zidutswazidutswa maguwa ofukizira
lubani amene anali pamwamba pake, ndipo anaphwanya mafano a Asera,
milungu ndi zifaniziro zake. Anaziperapera ndipo anaziwaza pamwamba
pa manda a amene ankapereka nsembe kwa mafanowo. [5] Iye anatentha
mafupa a ansembe pa maguwa awo, kotero iye anayeretsa Yuda ndi
Yerusalemu. [6] Ku mizinda ya Manase, Efereimu ndi Simeoni mpaka kufika
ku Nafutali, ndiponso malo a mabanja owazungulira, [7] iye anagwetsa
maguwa ansembe ndi mafano a Asera ndi kuphwanyaphwanya milungu
yawo kukhala fumbi ndi kuduladula maguwa ofukizapo lubani m'dziko
lonse la Israeli. Atatero, anabwerera ku Yerusalemu.

[8] M'chaka cha 18 cha ulamuliro wa Yosiya, atayeretsa dziko ndi
Yerusalemu, Yosiya anatuma Safani mwana wa Azariya ndi Maaseya,
wolamulira mzinda pamodzi ndi Yowa mwana wa Yowahazi mlembi
wolemba mbiri, kuti akonze Nyumba ya Yehova Mulungu wake.

[9] Iwo anapita kwa Hilikiya, mkulu wa ansembe ndipo anamupatsa
ndalama zimene zinaperekedwa m'Nyumba ya Mulungu, zimene Alevi
amene anali alonda apakhomo analandira kuchokera kwa anthu a ku
Manase, Efereimu ndi onse otsala a ku Israeli ndiponso anthu onse
ochokera ku Yuda ndi Benjamini ndi okhala mu Yerusalemu. [10] Ndipo
anazipereka m'manja mwa anthu amene anasankhidwa kuti ayang'anire
ntchito ya Nyumba ya Yehova. Anthu amenewa ankalipira antchito amene
ankakonzanso Nyumba ya Mulungu. [11] Iwo anaperekanso ndalama kwa
amisiri a matabwa ndi amisiri omanga nyumba kuti agule miyala yosema
ndi matabwa a phaso la nyumba ndi nsichi zomangira zomwe mfumu ya
Yuda inalekerera kuti zigwe ndi kuwonongeka.

[12] Anthuwa anagwira ntchitoyi mokhulupirika. Amene
ankawayang'anira anali Yahati ndi Obadiya, Alevi ochokera ku banja
la Merari, ndi Zekariya ndi Mesulamu ochokera ku banja la Kohati. Alevi
onse amene anali aluso loyimbira zida za nyimbo [13] ankayang'anira anthu
onyamula katundu, namatsogolera anthu onse amene ankagwira ntchito
iliyonse yotumikira. Alevi ena anali alembi, akapitawo ndiponso alonda
apamakomo.

### *Buku la Malamulo Lipezeka*

[14] Pa nthawi imene ankatulutsa ndalama zimene anabwera nazo ku
Nyumba ya Yehova, wansembe Hilikiya anapeza Buku la Malamulo limene
linaperekedwa kudzera mwa Mose. [15] Hilikiya anati kwa Safani, mlembi
wa zochitika, "Ine ndapeza Buku la Malamulo m'Nyumba ya Yehova." Iye
analipereka kwa Safani.

[16] Ndipo Safani anapita nalo bukulo kwa mfumu ndi kumufotokozera
kuti: "Akuluakulu anu akuchita zonse zimene zinapatsidwa kwa iwo.
[17] Iwo alipira ndalama zimene zinali m'Nyumba ya Yehova ndipo

azipereka kwa akapitawo ndi anthu antchito.” [18] Kenaka Safani, mlembi
wa zochitika anawuza mfumu, “Wansembe, Hilikiya wandipatsa ine buku
ili.” Ndipo Safani anawerenga bukulo pamaso pa mfumu.

[19] Mfumu itamva mawu a Buku la Malamulo, inang’amba mkanjo wake.
[20] Iye analamula izi kwa Hilikiya, Ahikamu mwana wa Safani, Abidoni
mwana wa Mika, Safani mlembi wa zochitika ndi Asaya mtumiki wa
mfumu: [21] “Pitani ndipo mukafunse Yehova m’malo mwanga ndi m’malo
mwa otsala a Israeli ndi Yuda za zimene zalembedwa m’buku limene
lapezekali. Mkwiyo wa Yehova ndi waukulu umene watsanulidwa pa
ife chifukwa makolo athu sanasunge mawu a Yehova. Iwo sanachite
motsatira zonse zimene zalembedwa m’buku ili.”

[22] Hilikiya pamodzi ndi anthu amene anawatuma aja, anapita
kukayankhula ndi mneneri wamkazi Hulida, amene anali mkazi wa
Salumu mwana wa Tokati, mwana wa Hasira, wosunga zovala zaufumu.
Hulida ankakhala mu Yerusalemu, m’dera lachiwiri la mzindawo.

[23] Iye anati kwa anthuwo, “Yehova Mulungu wa Israeli akuti, muwuzeni
munthu amene wakutumani kwa ineyo kuti, [24] ‘Yehova akunena kuti, Ine
ndidzabweretsa mavuto pamalo pano ndi pa anthu ake, matemberero
onse amene alembedwa m’bukuli amene awerengedwa pamaso pa mfumu
ya Yuda. [25] Chifukwa iwo anasiya Ine ndi kufukiza lubani kwa milungu
ina ndi kuwutsa mkwiyo wanga ndi zonse zimene manja awo anapanga,
mkwiyo wanga udzatsanulidwa pamalo pano ndipo sudzazimitsidwa.’
[26] Uzani mfumu ya Yuda imene yakutumani kuti mudzafunse kwa Yehova
Mulungu wa Israeli, ‘Chimene Yehova, Mulungu wa Israeli akunena
mokhudzana ndi mawu amene mwamva ndi ichi: [27] Pakuti mtima
wako walapa, ndipo wadzichepetsa wekha pamaso pa Mulungu pamene
unamva zimene Iye ananena motsutsa malo ano ndi anthu ake, ndipo
chifukwa iwe unadzichepetsa wekha pamaso pa Ine ndi kung’amba zovala
zako ndi kulira pamaso panga, ndamva pemphero lako, atero Yehova.
[28] Tsono Ine ndidzakutengera kwa makolo ako, ndipo udzayikidwa
m’manda mwamtendere. Maso ako sadzaona mavuto onse amene Ine
ndidzabweretsa pa malo ano ndi pa iwo amene amakhala pano.’ ”

Choncho iwo anatenga yankho lakelo ndi kubwerera kwa mfumu.

[29] Ndipo mfumu inasonkhanitsa pamodzi akuluakulu onse a Yuda ndi
Yerusalemu. [30] Iye anapita ku Nyumba ya Yehova pamodzi ndi anthu a
Yuda, anthu a mu Yerusalemu, ansembe ndi Alevi, anthu onse kuyambira
wamng’ono mpaka wamkulu. Iye anawerenga pamaso pawo mawu onse
a Buku la Chipangano, limene linapezeka m’Nyumba ya Yehova. [31] Mfumu
inayimirira pa chipilala chake ndipo inachitanso pangano pamaso pa
Yehova: kutsatira Yehova, ndi kusunga malamulo ake, machitidwe ake ndi
malangizo ake ndi mtima wake wonse ndi moyo wake wonse, ndi kumvera
mawu a pangano olembedwa m’bukulo.

[32] Tsono Yosiya anawuza aliyense amene anali mu Yerusalemu ndi
Benjamini kuti azisunga panganoli. Anthu a mu Yerusalemu anachita izi
motsata pangano la Mulungu, Mulungu wa makolo awo.

[33] Yosiya anachotsa mafano onse onyansa m’dziko lonse limene linali la
Aisraeli ndipo anawuza onse amene anali mu Israeli kutumikira Yehova
Mulungu wawo. Pa masiku onse a moyo wake, iye sanaleke kutsatira
Yehova, Mulungu wa makolo awo.

# 35

*Yosiya Achita Chikondwerero cha Paska*

[1] Yosiya anachita chikondwerero cha Paska wa Yehova mu Yerusalemu,
ndipo mwana wankhosa wa Paska anaphedwa pa tsiku la khumi ndi
chinayi la mwezi woyamba. [2] Iye anasankha ansembe pa maudindo
awo ndipo anawalimbikitsa pa ntchito ya m'nyumba ya Yehova. [3] Iye
anati kwa Alevi amene amalangiza Aisraeli onse omwe anadzipatula kwa
Yehova: Ikani bokosi lopatulika m'Nyumba ya Mulungu amene Solomoni
mwana wa Davide mfumu ya Israeli anamanga. Lisamanyamulidwe pa
mapewa anu. Tsopano tumikirani Yehova Mulungu wanu ndi anthu ake
Aisraeli. [4] Mukhale m'magulu anu molingana ndi mabanja anu, molingana
ndi momwe analembera Davide mfumu ya Israeli ndiponso mwana wake
Solomoni.

[5] "Muziyima ku malo opatulika pamodzi ndi gulu la Alevi oyimira gulu
lililonse laling'ono la mabanja a abale anu amene ndi anthu wamba.
[6] Muzipha ana ankhosa a Paska, muzidzipatula nokha ndi kuwakonzera
abale anu ana ankhosa awo, kuchita zimene Yehova analamulira mwa
Mose."

[7] Yosiya anapereka kwa anthu wamba onse ana ankhosa ndi ana ambuzi
okwanira 30,000 ndi ng'ombe zazimuna 3,000, zopereka za Paska zonse
zochokera pa chuma chake cha mfumu.

[8] Akuluakulu akenso anapereka mwaufulu kwa anthu ndi kwa ansembe
ndi Alevi. Hilikiya, Zekariya ndi Yehieli oyang'anira ntchito ya m'Nyumba
ya Mulungu anapereka kwa ansembe zopereka za Paska 2,600 ndi
ng'ombe 300. [9] Konaniya nayenso pamodzi ndi Semaya ndi Netaneli,
abale ake ndi Hasabiya, Yeiyeli ndi Yozabadi, atsogoleri a Alevi, anapereka
nsembe za Paska 5,000 ndi ng'ombe 500 kwa Alevi.

[10] Mwambo unakonzedwa ndipo ansembe anayima pamalo pawo
pamodzi ndi Alevi m'magulu awo monga mfumu inalamulira. [11] Ana
ankhosa a Paska anaphedwa ndipo ansembe anawaza magazi amene
anaperekedwa kwa iwo pamene Alevi anali kusenda nyamazo.
[12] Iwo anayika padera nsembe zopsereza kuti azipereke kwa magulu
ang'onoang'ono a mabanja a anthu kuti apereke kwa Yehova monga
zinalembedwa m'buku la Mose. Ndipo anachita chimodzimodzi ndi
ng'ombe. [13] Anawotcha nyama za Paska monga momwe zinalembedwera
ndi kuwiritsa zopereka zopatulika m'miphika, m'mitsuko ndi m'ziwaya
ndipo anazipereka mofulumira kwa anthu onse. [14] Izi zitatha, anakonza
zawo ndi za ansembe chifukwa ansembe, zidzukulu za Aaroni, anali
otanganidwa kupereka nsembe zopsereza ndi mafuta a nyama mpaka
madzulo. Choncho Alevi amakonza zawo ndi za ansembe, ana a Aaroni.

[15] Anthu oyimba nyimbo, zidzukulu za Asafu, anali pa malo awo potsata
zomwe analemba Davide, Asafu, Hemani ndi Yedutuni mlosi wa mfumu.
Alonda apazipata anali pa chipata chilichonse ndipo kunali kosafunika
kuti achoke pa ntchito yawo, poti abale awo Alevi ankawakonzera zonse.

[16] Kotero pa nthawi imeneyi ntchito yonse ya Yehova ya chikondw-
erero cha Paska ndi nsembe zopsereza pa guwa la Yehova inachitika
monga analamulira mfumu Yosiya. [17] Aisraeli amene analipo anachita
chikondwerero cha Paska pa nthawi imeneyi ndi kuchita mwambo wa
chikondwerero cha Buledi Wopanda Yisiti, kwa masiku asanu ndi awiri.
[18] Paska yofanana ndi iyi sinachitikepo ku Israeli kuyambira nthawi
ya Samueli ndipo palibe mmodzi mwa mafumu a Israeli anachitapo

chikondwerero cha Paska ngati anachitira Yosiya pamodzi ndi ansembe,
Alevi ndi Ayuda onse ndi Aisraeli amene anali pamodzi ndi anthu a mu
Yerusalemu. 19 Chikondwerero cha Paska ichi chinachitika m'chaka cha
18 cha ulamuliro wa Yosiya.

*Imfa ya Yosiya*

20 Zimenezi zitachitika, pamene Yosiya anakonzanso Nyumba ya Mu-
lungu, Neko mfumu ya Igupto inapita kukachita nkhondo ku Karikemesi
ku mtsinje wa Yufurate, ndipo Yosiya anapita kukamenyana naye. 21 Koma
Neko anatumiza amithenga kwa iye kunena kuti, "Kodi pali mkangano
wanji pakati pa iwe ndi ine, iwe mfumu ya Yuda? Ine sindikuthira
nkhondo iwe pa nthawi ino, koma nyumba imene ndili nayo pa nkhondo.
Mulungu wandiwuza kuti ndifulumize choncho leka kutsutsana ndi
Mulungu amene ali ndi ine, mwina adzakuwononga."
22 Komabe Yosiya sanatembenuke kumusiya iyeyo, koma anadzizim-
bayitsa ndi kukalowa m'nkhondo. Iye sanamvere zimene Neko ananena
molamulidwa ndi Mulungu koma anapita kukamenyana naye ku chigwa
ku Megido.
23 Anthu oponya mivi analasa mfumu Yosiya, ndipo iye anawuza
akuluakulu ake, "Chotseni. Ndavulazidwa kwambiri." 24 Choncho
anamuchotsa iye m'galeta lake, ndipo anamuyika m'galeta lina limene
anali nalo ndipo anabwera naye ku Yerusalemu kumene anamwalirira.
Iye anayikidwa m'manda a makolo ake. Ndipo Ayuda ndi Yerusalemu
yense anamulira.
25 Yeremiya anapeka nyimbo za maliro chifukwa cha Yosiya, ndipo
mpaka lero lino amuna ndi akazi onse oyimba amakumbukira Yosiya
pa nyimbo zawo za maliro. Izi zinakhala mwambo mu Israeli ndipo
zinalembedwa m'Nyimbo za Maliro.
26 Zochitika zina za ulamuliro wa Yosiya ndi ntchito za kudzipereka
kwake, monga zinalembedwa m'Malamulo a Yehova, 27 zochitika zonse,
kuyambira pachiyambi mpaka pa mapeto, zalembedwa m'buku la ma-
fumu a Israeli ndi Yuda.

# 36

1 Tsono anthu a m'dzikomo anatenga Yehowahazi mwana wa Yosiya
namuyika kukhala mfumu mu Yerusalemu m'malo mwa abambo ake.

*Yehowahazi Mfumu ya Yuda*

2 Yowahazi anali wa zaka 23 pamene anakhala mfumu ndipo anala-
mulira mu Yerusalemu kwa miyezi itatu. 3 Mfumu ya Igupto inamuchotsa
pa udindo wa ufumu mu Yerusalemu ndipo inakhometsa msonkho dziko
la Yuda wa makilogalamu 3,400 asiliva ndi agolide. 4 Mfumu ya Igupto
inakhazika Eliyakimu, m'bale wake wa Yehowahazi kukhala mfumu
ya Yuda ndi Yerusalemu ndipo anasintha dzina la Eliyakimu kukhala
Yehoyakimu. Koma Neko anatenga Yowahazi m'bale wake wa Eliyakimu
ndi kupita naye ku Igupto.

*Yehoyakimu Mfumu ya Yuda*

5 Yehoyakimu anali wa zaka 25 pamene anakhala mfumu, ndipo
analamulira mu Yerusalemu zaka 11. Iye anachita zoyipa pamaso pa
Yehova Mulungu wake. 6 Nebukadinezara, mfumu ya ku Babuloni
anachita naye nkhondo ndipo anamumanga ndi zingwe zamkuwa ndi
kumutenga kupita naye ku Babuloni. 7 Nebukadinezara anatenganso

zipangizo za ku Nyumba ya Yehova kupita nazo ku Babuloni ndipo
anaziyika m'nyumba ya Mulungu wake kumeneko.

8 Zochitika zina za pa ulamuliro wa Yehoyakimu, zinthu zonyansa
zimene anachita ndi zonse zinapezeka kuti zinali zomutsutsa zalembedwa
m'buku la mafumu a Israeli ndi Yuda. Ndipo Yehoyakini mwana wake
analowa ufumu m'malo mwake.

### *Yehoyakini Mfumu ya Yuda*

9 Yehoyakini anali ndi zaka 21 pamene anakhala mfumu ndipo
analamulira mu Yerusalemu kwa miyezi itatu ndi masiku khumi. Iye
anachita zoyipa pamaso pa Yehova. 10 Nthawi ya mphukira, mfumu
Nebukadinezara inayitanitsa Yehoyakini ndipo inapita naye ku Babuloni,
pamodzi ndi ziwiya zamtengowapatali za m'Nyumba ya Mulungu wa
Yehova, ndipo anayika Zedekiya malume wake kukhala mfumu ya Yuda
ndi Yerusalemu.

### *Zedekiya Mfumu ya Yuda*

11 Zedekiya anali ndi zaka 21 pamene ankakhala mfumu, ndipo
analamulira mu Yerusalemu zaka 11. 12 Iye anachita zoyipa pamaso pa
Yehova Mulungu wake ndipo sanadzichepetse yekha pamaso pa mneneri
Yeremiya amene ankayankhula mawu a Yehova. 13 Iye anawukiranso
mfumu Nebukadinezara amene anamulumbiritsa m'dzina la Mulungu.
Iyeyo anali wosamva ndipo anawumitsa mtima wake. Sanatembenukire
kwa Yehova Mulungu wa Israeli. 14 Kuwonjezera apo, atsogoleri onse a
ansembe ndi anthu ena anapitirapitira kukhala osakhulupirika, kutsatira
machitidwe onse onyansa a mitundu ina ndi kudetsa Nyumba ya Yehova
Mulungu wawo, imene anayipatula mu Yerusalemu.

### *Kugwetsedwa kwa Yerusalemu*

15 Yehova, Mulungu wa makolo awo, ankatumiza mawu kwa iwo kudz-
era kwa amithenga ake kawirikawiri, chifukwa ankawamvera chisoni
anthu ake ndi malo ake okhalapo. 16 Koma iwo ananyoza amithenga
a Mulungu, anapeputsa mawu awo ndipo ankaseka aneneri ake mpaka
anawutsa mkwiyo wa Yehova pa anthu ake ndipo panalibenso mankhwala
owachiritsa. 17 Yehova anabweretsa mfumu ya anthu a ku Babuloni, imene
inapha anyamata awo ndi lupanga ku malo opatulika, ndipo sanasiye kaya
mnyamata kapena mtsikana, wamkulu kapena wokalamba. Mulungu
anapereka onsewo kwa Nebukadinezara. 18 Iye ananyamula kupita nazo
ku Babuloni zipangizo zonse za m'Nyumba ya Yehova Mulungu wawo,
zazikulu ndi zazing'ono zomwe, ndi chuma cha m'Nyumba ya Yehova
ndiponso chuma cha mfumu ndi akuluakulu ake. 19 Iwo anayatsa moto
Nyumba ya Mulungu, ndipo anagwetsa makoma a Yerusalemu. Anatentha
moto nyumba zonse zaufumu ndipo anawononga chilichonse chimene
chinali chofunika.

20 Iye anagwira ukapolo anthu otsala amene anapulumuka ku lupanga
ndi kupita nawo ku Babuloni, ndipo anakhala antchito ake ndi ana
ake mpaka pamene ufumu wa Peresiya unakhazikitsidwa. 21 Dziko
linakondwera ndi masabata ake. Pa nthawi yonse ya chipasuko chake
nthaka inapuma, mpaka zaka 70 zinakwana pokwaniritsa mawu a Yehova
amene anayankhula kudzera mwa Yeremiya.

22 M'chaka choyamba cha Koresi mfumu ya Peresiya, pofuna kukwanir-
itsa mawu a Yehova amene anayankhula kudzera mwa Yeremiya, Yehova

anakhudza mtima wa mfumu ya Peresiya kuti alengeze mu ufumu wake wonse ndipo anazilemba:

23 Chimene mfumu Koresi ya Peresiya ikunena ndi ichi:

"Yehova, Mulungu wakumwamba wandipatsa ine mafumu onse a dziko lapansi ndipo wandisankha kuti ndimumangire Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu ku Yuda. Aliyense wa anthu ake pakati panu, Yehova Mulungu wake akhale naye, ndipo apite."

# Ezara

*Koresi Athandiza Ayuda Kubwerera Kwawo*

1 M'chaka choyamba cha ufumu wa Koresi mfumu ya Perisiya, po-
funa kukwaniritsa zimene anayankhula kudzera mwa Yeremiya, Yehova
anayika maganizo mu mtima mwa Koresi mfumu ya Perisiya kuti alengeze
m'dziko lake lonse ndi mawu apakamwa ngakhalenso ochita kulemba.
2 Iye anati, "Koresi mfumu ya Perisiya ikunena kuti,

" 'Yehova, Mulungu wakumwamba wandipatsa maufumu onse a
dziko lapansi, ndipo wandipatsa udindo woti ndimumangire Nyumba
ku Yerusalemu m'dziko la Yuda. 3 Aliyense wa inu amene ali wa
Yehova, Mulungu wakeyo akhale naye. Tsono aliyense wa inu apite
ku Yerusalemu, m'dziko la Yuda kuti akamange Nyumba ya Yehova,
Mulungu wa Israeli. Iyeyu ndi Mulungu amene ali mu Yerusalemu.
4 Ndipo kumalo kulikonse kumene otsalawo akukhala, athandizidwe ndi
eni dzikolo powapatsa siliva, golide, katundu ndi ziweto ndi zopereka za
ufulu zoti akapereke ku Nyumba ya Yehova imene ili ku Yerusalemu.' "

5 Choncho atsogoleri a mabanja afuko la Yuda ndi la Benjamini komanso
ansembe ndi Alevi, aliyense amene Mulungu anawutsa mtima wake,
anayamba kukonzeka kupita kukamanga Nyumba ya Yehova imene ili
ku Yerusalemu. 6 Onse oyandikana nawo anawathandiza powapatsa
ziwiya za siliva ndi zagolide, kuphatikizaponso katundu ndi ziweto,
ndiponso mphatso zamtengo wapatali, kuwonjezera pa zopereka zaufulu
zija. 7 Nayenso mfumu Koresi anatulutsa ziwiya za m'Nyumba ya
Yehova zimene Nebukadinezara anazitenga kuzichotsa ku Yerusalemu ndi
kuziyika m'nyumba ya milungu yake. 8 Koresi, mfumu ya ku Perisiya
inatulutsa ziwiyazi ndi kuzipereka kwa Miteridati, msungichuma amene
anaziwerenga pamaso pa Sesibazara nduna yayikulu ya dziko la Yuda.
9 Chiwerengerochi chinali motere:

| | |
|---|---|
| Mabeseni agolide | 30 |
| mabeseni asiliva | 1,000 |
| a zopereka | 29 |
| 10 timiphika tagolide | 230 |
| timiphika tasiliva | 410 |
| ziwiya zina | 1,000. |

11 Ziwiya zonse zagolide ndi siliva pamodzi zinalipo 5,400. Zonsezi
ndi zimene Sezi-Bazara anabwera nazo pamene otengedwa ukapolo aja
ankabwerera ku Yerusalemu kuchokera ku Babuloni.

## 2

*M'ndandanda wa Ayuda amene Anabwerera*

1 Awa ndi anthu a m'chigawo cha Yuda amene anabwerako ku ukapolo,
amene Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni anawagwira ukapolo ndi
kupita nawo ku Babuloni (iwo anabwerera ku Yerusalemu ndi ku Yuda,

aliyense ku mzinda wake. 2 Iwo anabwerera pamodzi ndi Zerubabeli,
Yesuwa, Nehemiya, Seruya, Reelaya, Mordekai, Bilisani, Misipara, Bigivai,
Rehumu ndi Baana).

Chiwerengero cha anthu aamuna a Israeli chinali chotere:

| | |
|---|---|
| 3 Zidzukulu za Parosi | 2,172 |
| 4 zidzukulu za Sefatiya | 372 |
| 5 zidzukulu za Ara | 775 |
| 6 zidzukulu za Pahati-Mowabu (zochokera kwa Yesuwa ndi Yowabu) | 2,812 |
| 7 zidzukulu za Elamu | 1,254 |
| 8 zidzukulu za Zatu | 945 |
| 9 zidzukulu za Zakai | 760 |
| 10 zidzukulu za Bani | 642 |
| 11 zidzukulu za Bebai | 623 |
| 12 zidzukulu za Azigadi | 1,222 |
| 13 zidzukulu za Adonikamu | 666 |
| 14 zidzukulu za Bigivai | 2,056 |
| 15 zidzukulu za Adini | 454 |
| 16 zidzukulu za Ateri (kudzera mwa Hezekiya) | 98 |
| 17 zidzukulu za Bezayi | 323 |
| 18 zidzukulu za Yora | 112 |
| 19 zidzukulu za Hasumu | 223 |
| 20 zidzukulu za Gibari | 95. |

| | |
|---|---|
| 21 Anthu a ku Betelehemu | 123 |
| 22 Anthu aamuna a ku Netofa | 56 |
| 23 Anthu aamuna a ku Anatoti | 128 |
| 24 Anthu aamuna a ku Azimaveti | 42 |
| 25 Anthu aamuna a ku Kiriati Yearimu, Kefira ndi Beeroti | 743 |
| 26 Anthu aamuna a ku Rama ndi Geba | 621 |
| 27 Anthu aamuna a ku Mikimasi | 122 |
| 28 Anthu aamuna a ku Beteli ndi Ai | 223 |
| 29 Anthu aamuna a ku Nebo | 52 |
| 30 Anthu aamuna a ku Magaibisi | 156 |
| 31 Anthu aamuna a ku Elamu wina | 1,254 |
| 32 Anthu aamuna a ku Harimu | 320 |
| 33 Anthu aamuna a ku Lodi, Hadidi ndi Ono | 725 |
| 34 Anthu aamuna a ku Yeriko | 345 |
| 35 Anthu aamuna a ku Sena | 3,630. |

36 Ansembe anali awa:

| | |
|---|---|
| Zidzukulu za Yedaya (kudzera mu banja la Yesuwa) | 973 |
| 37 Zidzukulu za Imeri | 1,052 |
| 38 Zidzukulu za Pasuri | 1,247 |
| 39 Zidzukulu za Harimu | 1,017. |

40 Alevi anali awa:

| | |
|---|---|
| Zidzukulu za Yesuwa ndi Kadimieli (kudzera mwa ana a Hodaviya) | 74. |

41 Anthu oyimba nyimbo anali awa:

| | |
|---|---|
| Zidzukulu za Asafu | 128. |

42 Alonda a ku Nyumba ya Mulungu anali awa:

| |
|---|
| Zidzukulu za Salumu, zidzukulu za Ateri, zidzukulu za Talimoni, zidzukulu za |

43 Otumikira ku Nyumba ya Mulungu anali awa:

| |
|---|
| Zidzukulu za |
| Ziha, zidzukulu za Hasufa, zidzukulu za Tabaoti, |
| 44 zidzukulu za Kerosi, zidzukulu za Siyaha, Padoni, |
| 45 zidzukulu za Lebana, zidzukulu za Hagaba, zidzukulu za Akubu, |
| 46 zidzukulu za Hagabu, zidzukulu za Salimayi, zidzukulu za Hanani, |
| 47 zidzukulu za Gideli, zidzukulu za Gahari, zidzukulu za Reaya, |
| 48 zidzukulu za Rezini, zidzukulu za Nekoda, zidzukulu za Gazamu, |
| 49 zidzukulu za Uza, zidzukulu za Peseya, zidzukulu za Besai, |
| 50 zidzukulu za Asina, zidzukulu za Meunimu, Nefusimu, |
| 51 zidzukulu za Bakibuku, zidzukulu za Hakufa, zidzukulu za Harihuri, |
| 52 zidzukulu za Baziruti, zidzukulu za Mehida, zidzukulu za Harisa, |
| 53 zidzukulu za Barikosi, zidzukulu za Sisera, zidzukulu za Tema, |
| 54 zidzukulu za Neziya ndi zidzukulu za Hatifa. |

55 Zidzukulu za antchito a Solomoni zinali izi:

| |
|---|
| Zidzukulu za |
| Sotai, zidzukulu za Hasofereti, zidzukulu za Peruda, |
| 56 zidzukulu za Yaala, zidzukulu za Darikoni, zidzukulu za Gideli, |
| 57 zidzukulu za Sefatiya, zidzukulu za Hatilu, |
| zidzukulu za Pokereti, Hazebayimu ndi Ami. |
| 58 Chiwerengero cha onse otumikira ku Nyumba ya Mulungu pamodzi ndi zidzu |

59 Anthu ali m'munsiwa anabwera kuchokera ku mizinda ya Teli-Mela,
Teli-Harisa, Kerubi, Adoni ndi Imeri, ngakhale samatha kutsimikiza kuti
mafuko awo analidi Aisraeli enieni kapena ayi:

| |
|---|
| 60 Zidzukulu za Delaya, zidzukulu za Tobiya, ndi zidzukulu za Nekoda. Onse pa |

61 Ndi ena pakati pa ansembe anali awa:

| Zidzukulu za |
|---|
| Hobiya, Hakozi, ndi Barizilai (Zidzukulu za Hobiya, zidzukulu za Hakozi ndi zi |

62 Amenewa anafufuza mayina awo m'buku lofotokoza mbiri ya mafuko
awo, koma mayinawo sanawapezemo, choncho anawachotsa pa un-
sembe ngati anthu odetsedwa pa zachipembedzo. 63 Bwanamkubwa
anawawuza anthuwo kuti asamadye nawo mpaka atapezeka wansembe
wodziwa kuwombeza ndi Urimu ndi Tumimu.

64 Chiwerengero cha anthu onse pamodzi chinali 42,360, 65 kuwonjezera
pamenepo, panalinso antchito awo aamuna ndi aakazi okwanira 7,337.
Analinso ndi amuna ndi akazi oyimba nyimbo okwanira 200. 66 Anali
ndi akavalo 736, nyulu 245, 67 ngamira 435 ndi abulu 6,720.

68 Atafika ku Nyumba ya Yehova mu Yerusalemu, ena mwa atsogoleri a
mabanja anapereka zopereka zaufulu zothandizira kumanganso Nyumba
ya Mulungu pamalo pake pakale. 69 Anapereka kwa msungichuma wa
ntchitoyo molingana ndi mmene aliyense chuma chake chinalili: golide
wa makilogalamu 500, siliva makilogalamu 2,800 ndi zovala za ansembe
zokwanira 100.
70 Ansembe, Alevi, oyimba nyimbo, alonda ndi antchito a ku Nyumba ya
Yehova pamodzi ndi Aisraeli ena onse ankakhala m'midzi ya makolo awo.

# 3

*Kumangidwanso kwa Guwa la Nsembe*

1 Utafika mwezi wa chisanu ndi chiwiri Aisraeli atakhala kale m'midzi
yawo, anthu anasonkhana ku Yerusalemu ndi cholinga chimodzi. 2 Kenaka
Yesuwa mwana wa Yozadaki ndi ansembe anzake pamodzi ndi Zerubabeli
mwana wa Sealatieli ndi abale ake anayamba kumanga guwa lansembe la
Mulungu wa Israeli. Anatero pofuna kuti aziperekapo nsembe zopsereza
monga analembera m'buku la Mose, munthu wa Mulungu uja. 3 Ndi man-
tha ndi mantha chifukwa cha anthu a m'mayikomo, iwo anamanga guwalo
pa maziko ake akale, ndipo anapereka nsembe zopsereza kwa Mulungu
pa guwapo mmawa ndi madzulo. 4 Ankasunga tsiku la chikondwerero cha
misasa monga momwe zinalembedwera. Ankaperekanso nsembe za tsiku
ndi tsiku monga mwa chiwerengero chake potsata mwambo wake wa tsiku
ndi tsiku monga zinalembedwa. 5 Pambuyo pake, ankapereka nsembe
zopsereza, nsembe zopereka pa nthawi ya mwezi watsopano ndi za pa
masiku onse a chikondwerero oyikidwa kutamandira Yehova, kudzanso
nsembe zaufulu zopereka kwa Yehova. 6 Kuyambira pa tsiku loyamba
la mwezi wachisanu ndi chiwiri, iwo anayambanso kupereka nsembe
zopsereza kwa Yehova, ngakhale kuti maziko a Nyumba ya Yehova anali
asanamangidwe.

*Kumangidwanso kwa Nyumba ya Mulungu*

7 Ndipo anapereka ndalama kwa amisiri a miyala ndi kwa amisiri a
matabwa, ndi chakudya, chakumwa ndi mafuta kwa anthu a ku Sidoni ndi
a ku Turo, kuti abweretse mitengo ya mkungudza pa nyanja kuchokera ku

Lebanoni mpaka ku Yopa. Zonsezi anachita malinga ndi chilolezo chimene analandira kuchokera kwa Koresi, mfumu ya Peresiya.
8 Tsono mu chaka chachiwiri atabwera ku Yerusalemu, ku malo akale a Nyumba ya Yehova, mwezi wachiwiri Zerubabeli mwana wa Sealatieli, Yesuwa mwana wa Yozadaki pamodzi ndi abale awo onse, ansembe, Alevi ndi onse amene anabwera ku Yerusalemu kuchokera ku ukapolo, anayamba kugwira ntchito. Iwo anasankha Alevi a zaka zoyambira makumi awiri kuti aziyang'anira ntchito ya kumanga Nyumba ya Yehova.
9 Yesuwa ndi ana ake aamuna kudzanso abale ake, Kadimieli ndi ana ake (ana a Yuda) onse pamodzi anasenza udindo woyang'anira antchito ku Nyumba ya Mulungu, kuphatikizanso ana a Henadadi komanso Alevi, ana awo ndi abale awo.
10 Amisiri omanga nyumba atamanga maziko a Nyumba ya Yehova, ansembe anabwera akuyimba malipenga, atavala zovala zaunsembe. Ndipo Alevi, zidzukulu za Asafu, anadza akuyimba matambolini ndi kutenga udindo wawo wotamanda Yehova, potsata malangizo a Davide
mfumu ya Aisraeli. 11 Iwo ankayimba motamanda ndi mothokoza Yehova nyimbo iyi:

"Yehova ndi wabwino;
chikondi chake pa Israeli ndi chamuyaya."

Ndipo anthu onse ankafuwula kwambiri kumutamanda Yehova, chifukwa
maziko a Nyumba ya Yehova anali kumangidwa. 12 Koma ambiri
mwa ansembe, Alevi ndiponso atsogoleri amabanja, akuluakulu amene anaona Nyumba ya Yehova yakale, analira mokweza pamene anaona maziko a nyumbayi akumangidwa. Komanso ena ambiri ankafuwula
mosangalala. 13 Choncho panalibe amene ankatha kusiyanitsa liwu lofuwula mokondwerera ndi liwu la anthu olira, chifukwa anthuwo ankafuwula kwambiri. Ndipo liwu lofuwulalo limamveka kutali.

# 4

## *Atsutsa za Kumanganso Nyumba ya Yehova*

1 Adani a Yuda ndi Benjamini anamva kuti anthu obwera ku ukapolo aja
akumangira Nyumba Yehova, Mulungu wa Israeli. 2 Tsono anapita kwa
Zerubabeli ndi kwa atsogoleri a mabanja awo ndi kunena kuti, "Mutilole kuti tikuthandizeni kumangaku chifukwa ife timapembedza Mulungu wanu monga momwe mumachitira inu, ndipo takhala tikupereka nsembe kwa Iye kuyambira nthawi ya Esrahadoni, mfumu ya ku Asiriya, amene anabwera nafe kuno."
3 Koma Zerubabeli, Yesuwa ndi atsogoleri ena otsala a mabanja a Aisraeli anayankha kuti, "Inu simungatithandize kumangira Nyumba Yehova, Mulungu wathu. Tokha tidzamumangira Nyumba Yehova, Mulungu wa Aisraeli, monga mfumu Koresi, mfumu ya Perisiya inatilamulira."
4 Tsono anthu a m'dzikomo anayamba kuchititsa ulesi anthu a ku Yuda, ndi
kuwachititsa mantha kuti aleke ntchito yomangayo. 5 Analemba alangizi
ena kuti alepheretse cholinga chawo pa ntchitoyo pa nthawi yonse ya Koresi, mfumu ya ku Perisiya, ndiponso mpaka pamene Dariyo mfumu ya ku Perisiya ankalamulira dzikolo.

## *Kutsutsa Kwina pa Nthawi ya Ahasiwero ndi Aritasasita*

6 Mfumu Ahasiwero atangoyamba kulamulira dzikolo, adani aja analemba kalata yoneneza anthu a Yuda ndi Yerusalemu.

7 Ndiponso m'nthawi ya Aritasasita mfumu ya Perisiya, Bisilamu, Mitiredati, Tabeeli ndi anzawo ena analemba kalata inanso kwa Aritasasita. Kalatayo inalembedwa m'Chiaramu ndipo ankatanthauzira poyiwerenga.

8 Rehumu mkulu wankhondo ndi Simisai mlembi, nawonso analemba kalata yawo yoneneza anthu a ku Yerusalemu kwa mfumu Aritasasita. Anayilemba motere:

9 Kalata yochokera kwa Rehumu, mkulu wa gulu lankhondo, mlembi Simisai ndi anzawo awa: oweruza, nduna, akuluakulu ena, anthu a ku
Peresiya, Ereki, Babuloni, Susa m'dziko la Elamu,
10 ndi mitundu ina imene mkulu wolemekezeka, Osanipara anayisamutsa ndi kuyikhazika m'mizinda ya Samariya ndi m'madera ena apatsidya la Yufurate.

11 Mawu a m'kalata ya kwa Aritasasita anali awa:

Kwa mfumu Aritasasita:

Kuchokera kwa atumiki anu, anthu a kutsidya kwa Yufurate:

12 Amfumu tati mudziwe kuti Ayuda amene anabwera kuno kuchokera kwanuko apita ku Yerusalemu ndipo akumanganso mzinda wa anthu owukira ndi oyipa uja. Akumaliza makoma ake ndipo akukonzanso maziko.
13 Kuwonjeza apo amfumu mudziwe kuti ngati amalize kumanganso mzindawu ndi kukonzanso makoma ake, adzaleka kukhoma msonkho, kulipira ndalama zakatundu olowa m'dziko kapena msonkho wina uliwonse, ndipo chuma cha thumba la ufumu chidzachepa.
14 Popeza tsono ife timadya nawo kwa mfumu sitiyenera tizingoonerera zinthu zochititsa mfumu manyazi. N'chifukwa chake tikutumiza uthenga kwa inu a mfumu kuti mudziwe zonse.
15 Choncho pachitike kafukufuku m'buku la mbiri yakale ya makolo anu. M'buku la mbiri zakale mudzapezamo ndi kuwerenga kuti mzinda umenewu ndi waupandu, wosautsa mafumu ndi nduna zam'madera zomwe. Kuyambira kale wakhala ukuwukira ulamuliro uliwonse. N'chifukwa chake mzinda umenewu anawuwononga.
16 Tsono tikukudziwitsani amfumu kuti ngati mzinda umenewu umangidwanso ndi makoma ake n'kutsirizidwanso ndiye kuti inu simudzalamuliranso chigawo cha patsidya pa Yufurate.
17 Mfumu inatumiza yankho ili:

Mkulu wa gulu lankhondo Rehumu, mlembi Simisai ndi anzanu onse amene akukhala ku Samariya ndi m'zigawo zina zonse za Patsidya pa Yufurate.

Landirani moni.

18 Kalata imene munatumiza ija yawerengedwa bwino lomwe pamaso panga.
19 Ine nditalamula kuti afufuze nkhaniyi kwapezekadi kuti mzinda umenewu uli ndi mbiri yowukira mafumu ndi kuti zaupandu ndi zowukira zinkachitikadi m'menemo.
20 Mafumu amphamvu akhala akulamulira Yerusalemu ndi chigawo chonse cha Patsidya pa Yufurate. Iwo ankalandira msonkho ndi kulipira ndalama zakatundu olowa m'dziko pa kanthu kena kalikonse.
21 Tsopano inu khazikitsani lamulo kuti anthu amenewo asiye ntchitoyo, asamangenso mzindawo mpaka ine nditalamula
22 Musachedwe kuchita zimenezi. Kodi ine ndingalole bwanji kuti zowononga zotere zikule ndi kupweteka ine mfumu?

23 Kalata ya mfumu Aritasasitayi itangowerengedwa pamaso pa Rehumu ndi Simisai mlembi uja, ndi anzawo onse, iwo anapita msangamsanga ku

Yerusalemu kukawaletsa Ayuda aja mwamphamvu kuti asapitirire ntchito yawo.

24 Motero ntchito yomanga Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu inayimitsidwa mpaka chaka cha chiwiri cha ulamuliro wa Dariyo mfumu ya ku Perisiya.

# 5

*Kalata ya Tatenai Yopita kwa Dariyo*

1 Nthawi imeneyo aneneri Hagai ndi Zekariya, mwana wa Ido,
ankayankhula kwa Ayuda okhala m'dziko la Yuda ndi mu Yerusalemu
m'dzina la Mulungu wa Israeli, amene anali nawo. 2 Pambuyo pake
Zerubabeli mwana wa Sealatieli ndi Yesuwa mwana wa Yozadaki ananyamuka nakayambanso kumanga Nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu. Ndipo aneneri a Mulungu anali nawo pamodzi, kuwathandiza.

3 Pa nthawi imeneyo Tatenai, bwanamkubwa wa chigawo cha patsidya pa Yufurate pamodzi ndi Setari-Bozenai ndi anzawo anapita kwa iwo ndi kukawafunsa kuti, "Anakulolani ndani kuti mumangenso Nyumba
imeneyi ndi kutsiriza khoma lake?" 4 Anawafunsanso kuti, "Kodi anthu
amene akumanga nyumbayi mayina awo ndani?" 5 Koma Mulungu wawo
amayang'anira atsogoleri Ayuda, motero kuti anthu aja anaganiza kuti asawaletse kumanga Nyumbayo mpaka atalembera mfumu Dariyo kalata ndi kulandira yankho lake.

6 Iyi ndi kalata imene Tatenai bwanamkubwa wa dera la patsidya pa Yufurate, ndiponso Setari-Bozenai ndi anzake, akazembe amene anali m'chigawo cha patsidya pa Yufurate, anatumiza kwa mfumu Dariyo
7 Analemba kalatayo motere:

Kwa mfumu Dariyo:
Mukhale ndi mtendere wonse.

8 Amfumu mudziwe kuti ife tinapita ku dziko la Yuda ku Nyumba ya Mulungu wamkulu. Nyumbayo ikumangidwa ndi miyala ikuluikulu ndipo akuyala matabwa pa makoma. Ntchitoyi ikugwiridwa mwachangu ndipo ikuyenda bwino kwambiri mwautsogoleri wawo.

9 Ndipo tinawafunsa atsogoleriwo kuti, "Anakulolezani kuti mumangenso
Nyumbayi ndi kutsiriza makoma ake ndani?" 10 Tinawafunsanso
mayina a atsogoleri awo, kuti tikalemba mayina atsogoleriwo tidzakudziwitseni kuti muwadziwe.

11 Yankho limene anatipatsa ndi ili:

"Ife ndife atumiki a Mulungu wa kumwamba ndi wa dziko lapansi, ndipo tikumanganso Nyumba imene mfumu ina yamphamvu ya
Israeli inamanga ndi kuyitsiriza zaka zambiri zapitazo. 12 Koma
chifukwa chakuti makolo athu anakwiyitsa Mulungu wakumwamba, Iye anawapereka kwa Nebukadinezara Mkalideya, mfumu ya Babuloni, amene anawononga Nyumbayi ndi kutenga anthu onse kupita nawo ku ukapolo ku Babuloni.

13 "Komabe chaka choyamba cha Koresi, mfumu ya ku Babuloni,
mfumu Koresiyo anapereka lamulo lakuti Nyumba ya Mulunguyi
imangidwenso. 14 Ndipo ziwiya zagolide ndi zasiliva za ku Nyumba

ya Mulungu zimene Nebukadinezara anazitenga m'Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu ndi kukaziyika m'nyumba ya milungu ya ku Babuloni, anakazichotsa ku nyumba ya milungu ya ku Babuloniko ndi kuzipereka kwa Sesibazara, amene mfumu inamusankha kukhala
bwanamkubwa. 15 Tsono mfumuyo inamuwuza kuti, 'Tenga ziwiyazi ukaziyike m'Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu. Ndipo Nyumba ya Mulunguyo ikamangidwenso pa maziko ake akale.'

16 "Choncho Sesibazarayo anabwera ndi kumanga maziko a Nyumba ya Mulunguyo mu Yerusalemu. Kuyambira tsiku limenelo mpaka lero yakhala ikumangidwa ndipo sinathebe."

17 N'chifukwa chake ngati chingakukomereni amfumu, pachitike kafukufuku m'nyumba yaufumu mosungira chuma ndi mabuku okhudza mbiri ya Babuloni kuti tione ngati mfumu Koresi inalamuladi za kumanganso Nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu. Kenaka amfumu mutiwuze zomwe zikukondweretsani kuti mugamule pa nkhani imeneyi.

# 6

*Lamulo la Mfumu Dariyo*

1 Atalandira mawuwo mfumu Dariyo anapereka lamulo ndipo kafukufuku anachitikadi ku Babuloni m'nyumba yosungira chuma ndi mabuku ambiri
yakale. 2 Ndipo ku Ekibatana, likulu la dera la Mediya, kunapezeka mpukutu mmene munalembedwa kuti,
Chikumbutso:

3 M'chaka choyamba cha ufumu wa Koresi, mfumuyo inapereka lamulo lokhudza Nyumba ya Mulungu mu Yerusalemu.

Analamula kuti Nyumba ya Mulungu imangidwenso kukhala malo woperekerako nsembe. Maziko ake amangidwe kolimba pa malo pomwe paja pali maziko ake akale ndipo mulitali mwake mukhale mamita 27,
mulifupi mwake mukhale mamita 27. 4 Mumange mizere itatu ya miyala yayikulu ndi mzere umodzi wa matabwa, ndalama zake zolipirira
ntchitoyo zichokere m'thumba la ufumu. 5 Ndipo ziwiya zagolide ndi zasiliva za ku Nyumba ya Mulungu zimene Nebukadinezara anatenga m'Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu kupita nazo ku Babuloni, zonsezi zibwezedwe ndipo zipite ku Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu. Chilichonse chikabwezedwe pamalo pake m'Nyumbayo.

6 Tsopano Tatenai, bwanamkubwa wa dera la Patsidya pa Yufurate ndiponso Setari-Bozenai pamodzi ndi anzanu muchokeko kumeneko.
7 Ntchito yomanga Nyumba ya Mulunguyi muyileke. Mulekeni bwanamkubwa wa Ayuda ndiponso akuluakulu a Ayuda kuti amangenso Nyumba ya Mulunguyo pamalo pake.

8 Kuwonjezera pamenepo, ndikukhazikitsa lamulo lonena za mmene mudzachitire ndi akuluakulu a Ayuda powathandiza kumanganso Nyumba ya Mulunguyo:

Anthuwa muwalipire msanga kuchokera m'thumba la ufumu, kuchotsa
pa msonkho wa dera la Patsidya pa Yufurate. 9 Ndipo zonse zofunikira monga, ana ang'ombe, nkhosa zazimuna, ana ankhosa aamuna zoperekera nsembe yopsereza kwa Mulungu wakumwamba, ndi tirigu, mchere, vinyo ndi mafuta monga mmene ansembe a ku Yerusalemu angafunire,

muziwapatsa zimenezo tsiku ndi tsiku ndipo musamalephere kutero.
10 Zikatero ndiye kuti azipereka nsembe za fungo lokomera Mulungu
wakumwamba ndi kupempherera moyo wa mfumu ndi ana ake.
11 Ndikulamulanso kuti ngati wina asintha zimene ndalamulazi, mtanda umodzi wa nyumba yake udzasololedwa ndi kumunkhomera pamenepo ndipo nyumba yake adzayisandutse dzala.
12 Mulungu amene anasankha kuti anthu azimupembedza pa malo amenewa, achotse mfumu iliyonse kapena munthu aliyense amene adzasinthe zimenezi kapena kuwononga Nyumba ya Mulungu ya ku Yerusalemuko.
Ine Dariyo ndikuyika lamuloli, aliyense alitsate mosamala kwambiri.

*Kutsiriza ndi Kupereka Nyumba ya Mulungu*

13 Tsono potsata zomwe analamula mfumu Dariyo, Tatenai bwanamkubwa
wa dera la Patsidya pa Yufurate, Setari-Bozenai ndi anzawo anatsatira
mosamala kwambiri zimene mfumu Dariyo analamula. 14 Ndipo aku-
luakulu a Ayuda anapitiriza ntchito yomanga ija molimbikitsidwa ndi
aneneri Hagai ndi Zekariya mwana wa Ido. Anamaliza ntchito yomanga
Nyumbayo, monga momwe Mulungu wa Israeli analamulira ndiponso
potsata lamulo la Koresi, Dariyo ndi Aritasasita, mafumu a ku Perisiya.
15 Anatsiriza kumanga Nyumbayo pa tsiku lachitatu la mwezi wa Adara
m'chaka chachisanu ndi chimodzi cha ulamuliro wa mfumu Dariyo.
16 Choncho Aisraeli, ansembe, Alevi ndi anthu ena onse amene anali
atabwerako ku ukapolo, anachita chikondwerero chopereka Nyumba ya
Mulungu mwachimwemwe. 17 Poporeka Nyumba ya Mulunguyi, anthu
anapereka nsembe za ng'ombe zazimuna 100, nkhosa zazimuna 200, ana
ankhosa aamuna 400. Anaperekanso mbuzi zazimuna 12 ngati nsembe
yopepesera machimo a anthu onse, potsata chiwerengero cha mafuko
a Israeli. 18 Ndipo anakhazikitsa ansembe ndi Alevi pa ntchito zawo
zotumikira Mulungu mu Yerusalemu monga zinalembedwera m'buku la
Mose.

*Paska*

19 Pa tsiku la khumi ndi chinayi la mwezi woyamba, obwera ku ukapolo
aja anachita chikondwerero cha Paska. 20 Ansembe ndi Alevi anali
atadziyeretsa ndipo onsewo anali oyeretsedwa. Alevi anapha mwana
wankhosa wa Paska kuphera onse amene anatuluka ku ukapolo, ansembe
anzawo ndi iwo eni. 21 Nkhosa ya Paskayo anayidya ndi Aisraeli onse
amene anatuluka ku ukapolo, wina aliyense amene anaphatikana nawo
atadziyeretsa ku zonyansa za mitundu ina ya anthu akunja a m'dzikomo
kuti apembedze Yehova Mulungu wa Israeli. 22 Choncho pa masiku
asanu ndi awiri anasangalala pa chikondwerero cha buledi wopanda yisiti,
chifukwa Yehova anawadzaza ndi chimwemwe. Iye anatembenuza mtima
wa mfumu ya ku Asiriya motero kuti iyo inakomera mtima Aisraeli ndi
kuwathandiza ntchito yomanga Nyumba ya Mulungu, Mulungu wa Israeli.

# 7

*Ezara Abwera ku Yerusalemu*

1 Zitatha izi, Aritasasita ali mfumu ya ku Perisiya, panali wansembe wina
dzina lake Ezara. Iyeyu abambo ake anali Seraya mwana wa Azariya,
mwana wa Hilikiya, 2 mwana wa Salumu, mwana wa Zadoki, mwana wa
Ahitubi, 3 mwana wa Amariya, mwana wa Azariya, mwana wa Merayoti,
4 mwana wa Zerahiya, mwana wa Uzi, mwana wa Buki, 5 mwana wa

Abisuwa, mwana wa Finehasi, mwana wa Eliezara, mwana wa Aaroni
mkulu wa ansembe uja. 6 Ezara ameneyu anabwera kuchokera ku
Babuloni. Iyeyu anali wophunzira kwambiri za malamulo a Mose, amene
Yehova Mulungu wa Israeli anapereka. Mfumu inamupatsa chilichonse
chimene anapempha pakuti dzanja la Yehova Mulungu wake linali pa iye.
7 Tsono m'chaka cha chisanu ndi chiwiri cha ufumu wa Aritasasita, Ezara
pamodzi ndi Aisraeli ena, kuphatikizapo ansembe, Alevi, oyimba nyimbo,
alonda, ndi anthu ogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu ananyamuka
kubwerera ku Yerusalemu.
8 Ezara anafika ku Yerusalemu pa mwezi wachisanu wa chaka chachisanu
ndi chiwiri cha mfumu. 9 Iye anayamba ulendo wochoka ku Babuloni
pa tsiku loyamba la mwezi woyamba, ndipo anafika ku Yerusalemu pa
tsiku loyamba la mwezi wachisanu chifukwa dzanja labwino la Mulungu
wake linali pa iye. 10 Popeza Ezara anadzipereka kuwerenga ndi kusunga
malamulo a Yehova, iye anafunitsitsa kuphunzitsa Aisraeli malamulo ndi
malangizo a Mulungu.

## *Kalata ya Aritasasita Yopita kwa Ezara*

11 Iyi ndi kalata imene mfumu Aritasasita anapereka kwa wansembe
Ezara, mlembi wa malamulo, munthu wophunzira kwambiri zokhudza
malamulo ndi malangizo amene Yehova anapereka kwa Aisraeli.
12 Ndine Aritasasita, mfumu ya mafumu.
Ndikulembera iwe Ezara wansembe ndi mlembi wa malamulo a Mulungu
Wakumwamba.
Malonje.

13 Tsopano ndikulamula kuti Mwisraeli aliyense, wansembe kapena Mlevi
wokhala m'dziko langa, amene akufuna kupita ku Yerusalemu ndi
iwe, apite. 14 Ine mfumu pamodzi ndi alangizi anga asanu ndi
awiri tikukutumani kuti mukafufuze za dziko la Yuda ndi mzinda
wa Yerusalemu kuti mukaone mmene anthu akutsatira malamulo a
Mulungu wanu, amene anawapereka kwa inu. 15 Utenge siliva ndi golide
zimene ine mfumu ndi alangizi anga tapereka mwa ufulu kwa Mulungu
wa Israeli, amene amakhala ku Yerusalemu. 16 Mutengenso siliva yense
ndi golide amene mungamupeze m'dziko lonse la Babuloni, ngakhalenso
zinthu zimene anthu pamodzi ndi ansembe adzapereka mwaufulu
kuperekera ku Nyumba ya Mulungu wawo ya ku Yerusalemu. 17 Ndi
ndalama zimenezi mudzaonetsetse kuti mwagula ng'ombe zazimuna,
nkhosa zazimuna ndi ana ankhosa aamuna pamodzi ndi zopereka
zake za chakudya ndi za chakumwa. Mudzapereke zimenezi pa guwa
lansembe la Nyumba ya Mulungu wanu ya ku Yerusalemu.
18 Ndalama zotsala mudzagwiritse ntchito zimene inuyo ndi abale anu
zikakukomerani malingana n'kufuna kwa Mulungu wanu. 19 Ziwiya
zonse zimene akupatsani kuti mukatumikire nazo m'Nyumba ya Mu-
lungu wanu, kaziperekeni kwa Mulungu ku Yerusalemu. 20 Ndipo chili-
chonse chimene chingafunike m'Nyumba ya Mulungu wanu, chimene
mudzapeze mpata wopereka, ndalama zake zogulira zidzachokere
m'thumba la chuma cha mfumu.
21 Tsopano Ine, mfumu Aritasasita, ndikulamula asungichuma onse a dera
la Patsidya pa Yufurate kuti, chilichonse chimene wansembe Ezara,
mlembi wa malamulo a Mulungu Wakumwamba adzapempha kwa inu,
mupatseni mwa msanga. 22 Ngakhale atafunika makilogalamu 3,400

asiliva, makilogalamu 10,000 a tirigu, malita 2,000 a vinyo, malita
2,000 a mafuta ndi mchere wochuluka motani, zonsezi mupereke
monga zingafunikire. 23 Chimene Mulungu Wakumwamba walamula,
chichitike mosamalitsa ku Nyumba ya Mulungu Wakumwamba kuopa
kuti mkwiyo wa Mulungu ungayakire mfumu, dziko lake ndi ana
ake. 24 Tikukudziwitsaninso kuti kudzakhala kosaloledwa kukhometsa
msonkho uliwonse anthu awa: ansembe, Alevi, oyimba nyimbo, alonda
kapena aliyense wogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu.
25 Ndipo iwe, Ezara, monga mwa nzeru za Mulungu wako zimene
uli nazo, usankhe oyendetsa zinthu ndi oweruza kuti azilamulira
anthu onse okhala ku dera la Patsidya pa Yufurate, onse amene
amadziwa malamulo a Mulungu wako. Ndipo uphunzitse aliyense
amene sawadziwa. 26 Ndipo amene sadzamvera lamulo la Mulungu
wako ndi lamulo la mfumu alangidwe kolimba kapena aphedwe kapena
achotsedwe m'dzikolo, kapena katundu wake alandidwe, kapena
aponyedwe m'ndende.
27 Ezara anati atamandike Yehova, Mulungu wa makolo athu, amene
wayika ichi mu mtima wa mfumu kuti alemekeze Nyumba ya Yehova ya
ku Yerusalemu m'njira imeneyi. 28 Ameneyonso waonetsa chikondi chake
chosasinthika kwa ine pamaso pa mfumu, alangizi ake ndi nduna zake
zamphamvu kuti andikomere mtima. Choncho ndinalimba mtima popeza
Yehova, Mulungu wanga anali nane, ndipo ndinasonkhanitsa atsogoleri
ambiri a Israeli kuti apite nane pamodzi.

# 8

*M'ndandanda wa Akuluakulu a Mabanja Amene Anabwera ndi Ezara*

1 Nawa mayina a atsogoleri a mabanja amene anabwera nane kuchokera
ku Babuloni nthawi ya ulamuliro wa mfumu Aritasasita:

2 Geresomu wa fuko la Finehasi;
Danieli wa fuko la Itamara;
Hatusi 3 mwana wa Sekaniya wa fuko la Davide;

Zekariya wa fuko la Parosi. Pamodzi ndi iyeyu panalembedwa anthu ena 150;
4 Elihunai mwana wa Zerahiya, wa fuko la Pahati-Mowabu. Pamodzi ndi iyeyu panalinso anthu ena 400.
5 Sekaniya, mwana wa Yahazieli wa fuko la Zatu. Pamodzi ndi iyeyu panalembedwanso anthu 300.
6 Ebedi, mwana wa Yonatani wa fuko la Adini. Pamodzi naye analembedwanso anthu ena makumi asanu.
7 Yesaiya, mwana wa Ataliya wa fuko la Elamu. Pamodzi naye panali anthu ena 70.
8 Zebadiya, mwana wa Mikayeli wa fuko la Sefatiya. Pamodzi naye panalinso anthu 80.
9 Obadiya, mwana wa Yehieli wa fuko la Yowabu. Pamodzi naye panalinso anthu 218.
10 Selomiti mwana wa Yosifiya wa fuko la Bani. Pamodzi ndi iyeyu panalinso anthu 160.
11 Zekariya, mwana wa Bebai wa fuko la Babai. Pamodzi naye analembedwanso anthu 28.

12 Yohanani, mwana wa Hakatani wa fuko la Azigadi. Pamodzi naye panalinso anthu 110.
13 Atsogoleri a fuko la Adonikamu, anthu amene anabwera pambuyo pake mayina awo anali Elifeleti, Yeiyeli ndi Semaya. Pamodzi ndi iwowa panalinso anthu 60.
14 Atsogoleri a fuko la Bigivai anali Utai ndi Zakuri. Pamodzi ndi iwowa panali anthu 70.

*Kubwerera ku Yerusalemu*

15 Anthu onse ndinawasonkhanitsa ku mtsinje umene umapita mpaka ku
Ahava, ndipo kumeneko tinagona m'misasa masiku atatu. Nditayang'ana
pakati pa anthu ndi ansembe, ndinapeza kuti panalibe Alevi. 16 Choncho
ndinayitana atsogoleri awa: Eliezara, Arieli, Semaiya, Elinatani, Yaribu,
Elinatani, Natani, Zekariya ndi Mesulamu, pamodzi ndi aphunzitsi awiri,
Yoyaribu ndi Elinatani, 17 ndipo ndinawatuma kwa Ido, mtsogoleri wa
malo otchedwa Kasifiya. Ine ndinawawuza zoti akanene kwa Ido ndi
kwa abale ake, ogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu ku Kasifiyako,
kuti atitumizire anthu odzatumikira ku Nyumba ya Mulungu. 18 Chifukwa
cha kutikomera mtima kwa Mulungu wathu, Ido anatitumizira munthu
wanzeru, Serabiya, wa fuko la Mahili, mwana wa Levi, mwana wa Israeli,
pamodzi ndi ana ake aamuna ndi abale ake, anthu 18. 19 Anatitumiziranso
Hasabiya ndi Yesaiya wa fuko la Merari pamodzi ndi abale ake ndi
adzukulu ake, anthu makumi awiri. 20 Panalinso anthu ena 220 mwa
anthu ogwira ntchito m'Nyumba ya Mulungu amene Davide ndi nduna
zake anawasankha kuti azitumikira Alevi. Anthu onsewa analembedwa
potsata mayina awo.

21 Ku mtsinje wa Ahava, ndinalengeza kuti anthu onse asale zakudya,
adzichepetse pamaso pa Mulungu wathu ndi kupempha kuti atiyendetse
bwino ife ndi ana athu, ndi kuteteza katundu wathu yense. 22 Ine ndinali
ndi manyazi kupempha mfumu kuti atipatse asilikali oyenda pansi ndi
ena okwera pa akavalo kuti atiteteze kwa adani athu pa ulendo wathuwu
popeza tinali titawuza kale mfumu kuti "Yehova amateteza aliyense
amene amamudalira, koma amakwiyira onse amene amamukana."
23 Choncho tinasala zakudya ndi kupemphera kwa Mulungu wathu kuti
atiteteze ndipo Iye anamva pemphero lathu.

24 Tsono ndinasankha atsogoleri a ansembe khumi ndi awiri awa,
Serebiya, Hasabiya ndi abale awo khumi 25 ndipo ndinawayezera siliva ndi
golide, ndiponso ziwiya ndi zopereka za ku Nyumba ya Mulungu wathu
zimene mfumu ndi alangizi ake, nduna zake ndi Aisraeli onse amene
anali kumeneko anazipereka. 26 Nditayeza zonse, ndinapereka m'manja
mwawo, matani 22 asiliva, ziwiya zasiliva zolemera makilogalamu 70,
ndiponso makilogalamu 3,400 a golide, 27 mbale zagolide makumi awiri
zolemera makilogalamu asanu ndi atatu ndi theka ndiponso ziwiya ziwiri
zamkuwa wosalala, wonyezimira bwino ngati golide wamtengowapatali.

28 Kenaka ndinawawuza kuti, "Inu ndi opatulika a Yehova, ndiponso
mphatso zonsezi ndi zopatulika. Siliva ndi golideyu ndi zopereka zaufulu
kwa Yehova, Mulungu wa makolo anu. 29 Muzisamale bwino mpaka
mutaziyeza pamaso pa atsogoleri a ansembe ndi Alevi ndi akulu a mabanja
a Israeli m'zipinda za m'Nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu." 30 Choncho
ansembe ndi Alevi analandira zonse zoyezedwa zija, siliva, golide pamodzi
ndi ziwiya kuti apite nazo ku Nyumba ya Yehova ku Yerusalemu.

31 Pa tsiku la khumi ndi chiwiri la mwezi woyamba, tinachoka ku mtsinje
wa Ahava kupita ku Yerusalemu. Ndipo Mulungu wathu anali nafe, ndipo
anatiteteza kwa adani athu makamaka otibisalira pa njira. 32 Tinafika ku
Yerusalemu, komwe tinapumula masiku atatu.

33 Pa tsiku la chinayi lake, m'Nyumba ya Mulungu wathu, tinayeza siliva ndi golide ndi ziwiya zija n'kuzipereka m'manja mwa Meremoti mwana wa wansembe Uriya. Pamodzi ndi iyeyo panali Eliezara mwana wa Finehasi ndiponso Alevi awa: Yozabadi mwana wa Yesuwa ndi Nowadiya
mwana wa Binuyi. 34 Zonsezi anaziwerenga ndi kuziyeza ndipo analemba
kulemera kwa chinthu chilichonse.

35 Pamenepo anthu amene anatengedwa ukapolo aja anabwerera, anapereka nsembe zopsereza kwa Mulungu wa Israeli: ng'ombe zazimuna khumi ndi ziwiri, kuperekera Aisraeli onse, nkhosa zazimuna 96, ana ankhosa 77, ndiponso mbuzi zazimuna khumi ndi ziwiri ngati nsembe yopepesera machimo. Zonsezi zinali nsembe yopsereza zopereka kwa
Yehova. 36 Iwo anaperekanso chidziwitso cha mfumu chija kwa akulu-
akulu a mfumu ndi kwa akazembe a m'dera la Patsidya pa Yufurate. Pamenepo iwo anathandiza Ayuda ndiponso ntchito za pa Nyumba ya Mulungu.

# 9

*Pemphero la Ezara pa za Kukwatirana ndi a Mitundu Ina*

1 Zitachitika izi, atsogoleri anabwera kwa ine nati, "Aisraeli, kuphatik-
izanso ansembe ndi Alevi, sanadzipatule ku makhalidwe onyansa a anthu
a mitundu ina amene ayandikana nafe: Akanaani, Ahiti, Aperezi, Ayebusi,
Aamoni, Amowabu, Aigupto ndi Aamori. 2 Zomwe zikuchitika ndi izi.
Aisraeli ena ndi ana awo aamuna anayamba kukwatira ana aakazi a anthuwa. Choncho mtundu wopatulika wadzisokoneza ndi mitundu ya anthu a m'derali. Ndipo atsogoleri ndi akuluakulu ndiwo akupambana pa makhalidwe osakhulupirikawa."

3 Nditamva zimenezi, ndinang'amba chovala changa ndi mwinjiro wanga
ndipo ndinamwetula tsitsi la kumutu kwanga ndi ndevu zanga n'kukhala
pansi ndili wokhumudwa. 4 Ndinakhala pansi chomwecho wokhumudwa
mpaka nthawi ya nsembe ya madzulo. Ndipo onse amene ankaopa mawu a Mulungu wa Israeli chifukwa cha kusakhulupirika kwa anthu obwerako ku ukapolo anayamba kubwera kwa ine kudzasonkhana.

5 Ndipo pa nthawi ya nsembe ya madzulo, ndinadzidzimuka mu mtima wanga wokhumudwa n'kuyimirira, zovala zanga ndi mwinjiro wanga zikanali zong'ambika ndipo ndinagwada ndi kukweza manja anga kwa
Yehova Mulungu wanga 6 ndipo ndinapemphera kuti,
"Inu Mulungu wanga, ndine wamanyazi ndi wachisoni moti sindingathe kukweza nkhope yanga kwa Inu Mulungu wanga, chifukwa machimo athu akwera kupambana mitu yathu, ndipo kulakwa kwathu kwafika ku
thambo. 7 Ndipo chifukwa cha machimo athu, ifeyo, mafumu athu, ndi
ansembe athu takhala akutipereka m'manja mwa mafumu a mitundu ina ya anthu kuti atiphe pa nkhondo, atitenge ku ukapolo, atilande zinthu zathu ndi kutichititsa manyazi monga zilili leromu.

8 "Koma tsopano, pa kanthawi kochepa, Inu Yehova Mulungu wathu mwaonetsa kukoma mtima. Inu mwalola kuti ena mwa ife tipulumuke ku ukapolo ndi kutipatsa cholowa m'malo anu oyera. Mwatipulumutsa ku ukapolo ndi kutipatsa mpumulo pang'ono mu ukapolo wathu.

9 Ndifedi akapolo. Koma Inu Yehova simunatileke mu ukapolo wathu.
Mwationetsa chikondi chanu chosasinthika pamaso pa mafumu a ku
Perisiya. Mwatitsitsimutsa kuti timange Nyumba yanu pokonzanso
mabwinja ake. Mwatitchinjiriza m'dziko la Yuda ndi Yerusalemu.
10 "Koma tsopano, Inu Mulungu wathu, kodi tinganene chiyani titachita
zoyipa zonsezi? Ife taphwanya malamulo anu 11 amene munawapereka
kudzera mwa atumiki anu aneneri. Inu munati, 'Dziko limene
mukulowamolo kuti likhale cholowa chanu, ndi dziko lodetsedwa ndi
zonyansa za mitundu ya m'mayikomo. Ndipo adzaza dzikolo ndi
zochita zawo zonyansa. 12 N'chifukwa chake, musapereke ana anu
aakazi kuti akwatiwe ndi ana awo aamuna kapena kulola kuti ana awo
aakazi akwatiwe ndi ana anu aamuna. Musagwirizane nawo, kapena
kuchita nawo malonda kuti mukhale amphamvu ndi kudya zokoma za
m'dzikomo ndi kusiyira ana anu dzikoli ngati cholowa chawo mpaka
kalekale.'
13 "Tsono pambuyo pa zonse zimene zatigwera chifukwa cha ntchito
zathu zoyipa ndi uchimo wathu waukulu, komanso pambuyo poona
kuti Inu Mulungu wathu simunangotilanga kokha pang'ono kuyerekeza
ndi kuchimwa kwathu komanso mwalola kuti ena mwa ife tipulumuke,
14 kodi ife n'kuphwanyanso malamulo anu ndi kukwatirana ndi anthu
amitundu ina amene amachita zonyansa zimenezi? Kodi simudzatik-
wiyira ndi kutiwononga kwathunthu popanda wina wotsala kapena
wopulumuka? 15 Inu Yehova, Mulungu wa Israeli, ndinu wachifundo,
pakuti ndife otsala amene tapulumuka monga mmene zilili lero lino.
Ife tayima pamaso panu ngakhale tikudziwa kuchimwa kwathu pakuti
palibe munthu amene angathe kuyima pamaso panu chifukwa cha
machimo ake."

# 10

*Anthu Avomereza Tchimo Lawo*

1 Pamene Ezara ankapemphera ndi kuvomereza tchimo lawo, akulira
ndipo atadzigwetsa pansi ku Nyumba ya Mulungu, anthu ambiri an-
abwera kwa iye kudzasonkhana naye. Panali amuna, akazi ndi ana,
kuchokera m'dziko lonse la Israeli ndipo ankalira kwambiri. 2 Ndipo
Sekaniya, mwana wa Yehieli, wa fuko la Elamu, anawuza Ezara kuti, "Ife
takhala osakhulupirika kwa Mulungu wathu ndipo takhala tikukwatira
akazi achilendo a mayiko akunowa. Koma ngakhale zili chomwechi,
chikhulupiriro chilipobe pakati pa Aisraeli. 3 Tsopano tiyeni tichite naye
pangano Mulungu wathu, kuti tichotse akazi onsewa ndi ana awo, potsata
malangizo a inu mbuye wanga ndi wa anthu amene amaopa malamulo
a Mulungu wathu. Lolani kuti zichitike motsatira malamulo. 4 Tsono
dzukani, imeneyi ndi ntchito yanu. Ife tikuthandizani. Limbani mtima
ndipo gwirani ntchitoyi."
5 Choncho Ezara anayimirira ndipo analumbiritsa akulu a ansembe, Alevi
ndi Aisraeli onse, kuti adzachitedi monga Sekaniya ananenera. Tsono onse
analumbira. 6 Ezara anachoka ku Nyumba ya Mulungu napita ku chipinda
cha Yehohanani, mwana wa Eliyasibu. Anatandala kumeneko usiku wonse
ndipo sanadye chakudya kapena kumwa madzi popeza ankalira chifukwa
cha kusankhulupirika kwa anthu obwera ku ukapolo.
7 Tsono anthu analengeza m'dziko lonse la Yuda ndi m'mizinda yonse
ya Yerusalemu kwa onse ochokera ku ukapolo aja kuti asonkhane ku
Yerusalemu. 8 Ananena kuti wina aliyense amene saonekera pakutha pa

masiku atatu, adzalandidwa katundu wake, potsata malangizo a nduna ndi akuluakulu, ndipo adzachotsedwa m'gulu la anthu obwerako ku ukapolo.

9 Choncho anthu onse a m'dziko la Yuda ndi a m'dziko la Benjamini
anasonkhana ku Yerusalemu asanathe masiku atatu. Limeneli linali
tsiku la 20 la mwezi wa 9. Anthu onse anakhala pansi pa bwalo la
Nyumba ya Mulungu akunjenjemera chifukwa cha mvula yambiri imene
inagwa. 10 Ndipo wansembe Ezara anayimirira nawuza anthuwo kuti,
"Inu mwachimwa pomakwatira akazi achikunja ndi kumawonjezera pa
tchimo la Aisraeli. 11 Tsopano lapani kwa Yehova, Mulungu wa makolo
anu ndi kuchita zimene akufuna. Dzipatuleni kwa anthu a mayiko enawa
ndi kwa akazi achikunjawa."

12 Gulu lonse la anthu linayankha ndi mawu ofuwula kuti, "N'zoona!
Tichita monga mwaneneramu. 13 Koma pano pali anthu ambiri ndiponso
mvula ikugwa kwambiri, choncho sitingakayime panja. Ndiponso ntchi-
toyi si ya tsiku limodzi kapena awiri, chifukwa tachimwa kwambiri pa
zimene tachitazi. 14 Tsono mulole kuti atsogoleri athu ayimirire m'malo
mwa anthu onse. Aliyense wa m'mizinda yathu amene anakwatira
mkazi wachikunja abwere pa nthawi imene inu munene, ndipo abwere
pamodzi ndi akuluakulu ndi oweruza a mzindawo. Choncho mkwiyo wa
Mulungu wathu udzatichoka." 15 Koma Yonatani yekha mwana wa Asaheli
ndi Yahazieli mwana wa Tikiva ndiwo anatsutsapo pa zimenezi. Tsono
Mesulamu ndi Mlevi Sebetai anawayikira kumbuyo.

16 Choncho anthu obwerako ku ukapolo aja anachita zimene zimafunika.
Ndipo wansembe Ezara anasankha amuna amene anali atsogoleri a
mabanja potsata mafuko awo ndipo onsewo analembedwa mayina awo.
Tsiku loyamba la mwezi wa khumi anayambapo kuyifufuza nkhani
imeneyi. 17 Ndipo pofika tsiku loyamba la mwezi woyamba anali atathana
nawo anthu amene anakwatira akazi achilendo aja.

## *Okwatira Akazi Achilendo*

18 Nawu m'ndandanda wa ansembe amene anakwatira akazi achikunja:

Pa banja la Yesuwa ndi abale ake, ana a Yozadaki, panali awa: Maaseiya,
Eliezara, Yaribu ndi Gedaliya. 19 Iwo anatsimikiza zochotsa akazi
awo ndipo chifukwa cha kulakwa kwawo aliyense anapereka nkhosa
yayimuna ngati nsembe yopepesera machimo.

20 Pa banja la Imeri panali awa:
Hanani ndi Zebadiya.
21 Pa banja la Harimu panali awa:
Maseya, Eliya, Semaya, Yehieli ndi Uziya.
22 Pa banja la Pasuri panali awa:
Eliyoenai, Maseya, Ismaeli, Netaneli, Yozabadi ndi Eleasa.

23 Pakati pa Alevi panali:

Yozabadi, Simei, Kelaya (ndiye kuti, Kelita). Petaya, Yuda ndi Eliezara.
24 Pakati pa oyimba nyimbo panali
Eliyasibu.
Ochokera kwa alonda a zipata:
Salumu, Telemu ndi Uri.

25 Ochokera pakati pa Aisraeli ena:

a fuko la Parosi anali
Ramiya, Iziya, Malikiya, Miyamini, Eliezara, ndi Benaya.
26 A fuko la Elamu anali
Mataniya, Zekariya, Yehieli, Abidi, Yeremoti ndi Eliya.
27 A fuko la Zatu anali
Eliyoenai, Eliyasibu, Mataniya, Yeremoti, Zabadi ndi Aziza.
28 A fuko la Bebai anali
Yehohanani, Hananiya, Zabayi ndi Atilayi.
29 A fuko la Bani anali
Mesulamu, Maluki, Adaya, Yasubu, Seali ndi Yeremoti.
30 A fuko la Pahati-Mowabu anali
Adina, Kelali, Benaya, Maseya, Mataniya, Bezaleli, Binuyi ndi Manase.
31 A fuko la Harimu anali
Eliezara, Isiya, Malikiya, Semaya, Simeoni, 32 Benjamini, Maluki ndi Semariya.
33 A fuko la Hasumu anali
Mataneyi, Matata, Zabadi, Elifeleti, Yeremayi, Manase ndi Simei.
34 A fuko la Bani anali
Madai, Amramu, Uweli, 35 Benaya, Bediya, Keluhi, 36 Vaniya, Meremoti,
Eliyasibu, 37 Mataniya, Matenayi ndi Yasu.
38 A fuko la Binuyi anali
Simei, 39 Selemiya, Natani, Adaya, 40 Makinadebayi, Sasai, Sarai, 41 Azaleli,
Selemiya, Semariya, 42 Salumu, Amariya ndi Yosefe.
43 A fuko la Nebo anali
Yeiyeli, Matitiya, Zabadi, Zebina, Yadai, Yoweli ndi Benaya.

44 Onsewa anakwatira akazi achilendo. Tsono anawasudzula akaziwo ndi kuwatumiza kwawo pamodzi ndi ana awo.

# Nehemiya

*Pemphero la Nehemiya*

1 Awa ndi mawu a Nehemiya mwana wa Hakaliya:

Pa mwezi wa Kisilevi, chaka cha makumi awiri, pamene ndinali mu
mzinda wa Susa, 2 Hanani mmodzi mwa abale anga, anabwera ndi anthu
ena kuchokera ku Yuda, ndipo ine ndinawafunsa za Ayuda otsala amene
sanatengedwe ukapolo, ndiponso za mzinda wa Yerusalemu.
3 Anandiyankha kuti, "Amene sanatengedwe ukapolo aja ali pa mavuto
aakulu ndipo ali ndi manyazi. Khoma la Yerusalemu ndilogamukagamuka
ndipo zipata zake zinatenthedwa ndi moto."
4 Nditamva zimenezi, ndinakhala pansi ndi kuyamba kulira. Ndinalira
kwa masiku angapo. Ndinkasala zakudya ndi kumapemphera pamaso pa
Mulungu Wakumwamba. 5 Ndinkati:

"Inu Yehova, Mulungu wakumwamba, Mulungu wamkulu ndi
woopsa. Mumasunga pangano ndi kuonetsa chikondi chosasinthika kwa
onse amene amakukondani ndi kumvera malamulo anu. 6 Tcherani
khutu lanu ndi kutsekula maso anu kuti mumve pemphero la mtu-
miki wanune limene ndikupemphera usana ndi usiku pamaso panu
kupempherera Aisraeli, atumiki anu. Ndikuvomereza machimo a
Aisraeli amene tinakuchimwirani. Ndithu, ine ndi banja la makolo anga
tinakuchimwirani. 7 Ife tinakuchitirani zoyipa zambiri. Sitinamvere
mawu anu, malamulo ndi malangizo anu amene munapereka kwa
mtumiki wanu Mose.

8 "Kumbukirani mawu amene munawuza mtumiki wanu Mose akuti,
'Ngati mukhala osakhulupirika, ndidzakubalalitsani pakati pa mitundu
ina. 9 Koma mukabwerera kwa Ine, mukamvera malamulo anga ndi
kuwatsatadi, ndiye kuti ngakhale anthu anu atabalalika kutali chotani,
Ine ndidzawasonkhanitsa kuchokera kumeneko ndi kubwera nawo ku
malo amene ndinasankha kuti azidzayitanira dzina langa.'

10 "Iwo ndi atumiki anu ndi anthu anu, amene munawawombola
ndi mphamvu yanu yayikulu ndi dzanja lanu lamphamvu. 11 Inu
Ambuye tcherani khutu lanu kuti mumve pemphero la mtumiki wanune
ndiponso pemphero la atumiki anu amene amakondwera kuchitira
ulemu dzina lanu. Lolani kuti mtumiki wanune zinthu zindiyendere
bwino lero ndi kuti mfumu indichitire chifundo."

Nthawi imeneyi n'kuti ndili woperekera zakumwa kwa mfumu.

## 2

*Aritasasita Atumiza Nehemiya ku Yerusalemu*

1 Pa mwezi wa Nisani, m'chaka cha makumi awiri cha ufumu wa
Aritasasita, atabwera ndi vinyo pamaso pa mfumu ine ndinatenga vinyoyo
ndi kupereka kwa mfumu. Koma ndinali ndisanakhalepo ndi nkhope
yachisoni pamaso pake. 2 Tsono mfumu inandifunsa kuti, "N'chifukwa
chiyani nkhope yako ikuoneka yachisoni pamene iwe sukudwala? Ichi si
chinthu china koma chisoni cha mu mtima."

Ine ndinachita mantha kwambiri. 3 Ndinawuza mfumu kuti, "Mfumu
ikhale ndi moyo wamuyaya! Kodi nkhope yanga ilekerenji kuoneka

yachisoni pamene mzinda umene kuli manda a makolo anga, wasanduka
bwinja ndipo zipata zake zinawonongedwa ndi moto?"

4 Apo mfumu inandifunsa kuti, "Tsono ukufuna kundipempha chiyani?"

Ndipo ine ndinapemphera kwa Mulungu Wakumwamba. 5 Ndipo
ndinayankha kuti, "Ngati amfumu chingakukondweretseni, ngati
mungakomere mtima mtumiki wanune, mundilole kuti ndipite ku Yuda,
ku mzinda kumene kuli manda a makolo anga kuti ndikawumangenso."

6 Tsono mfumu, mfumukazi itakhala pambali pake, anandifunsa kuti,
"Kodi kumeneko ukakhalako masiku angati ndipo udzabwera liti?"
Ndinayiwuza mfumu nthawi yake ndipo inandilola kuti ndipite.

7 Ndipo ndinatinso kwa mfumu, "Ngati zikondweretse mfumu, mundi-
patse makalata oti ndikapereke kwa abwanamkubwa a ku chigawo cha
Patsidya pa Yufurate, kuti akandilole kudutsa mwamtendere mpaka
nditakafika ku Yuda. 8 Mundipatsenso kalata yokapereka kwa Asafu
woyang'anira nkhalango ya mfumu, kuti akandipatse mitengo yoka-
pangira mitanda ya zipata za nsanja yoteteza Nyumba ya Mulungu,
mitanda ya khoma la mzinda ndi ya nyumba yokhalamo ine." Mfumu
indipatse zomwe ndinapempha popeza Yehova wokoma mtima anali
nane. 9 Choncho ndinanyamuka ulendo wanga ndipo ndinafika kwa
abwanamkubwa a chigawo cha Patsidya pa Yufurate ndipo ndinawapatsa
makalata a mfumu. Mfumu n'kuti itatumiza akulu ankhondo ndi okwera
pa akavalo kuti atsagane nane.

10 Sanibalati wa ku Horoni ndi Tobiya wa ku Amoni atamva zimenezi,
iwo anayipidwa kwambiri kuti wina wabwera kudzachitira zabwino
Aisraeli.

### *Nehemiya Ayendera Makoma a Yerusalemu*

11 Ndinafika ku Yerusalemu, ndipo ndinakhala kumeneko masiku atatu.
12 Sindinawuze munthu aliyense za zimene Yehova anayika mu mtima
mwanga kuti ndichitire mzinda wa Yerusalemu. Choncho ndinanyamuka
usiku pamodzi ndi anthu ena owerengeka. Ndinalibe bulu wina aliyense
kupatula amene ndinakwerapo.

13 Ndinatuluka usiku podzera ku Chipata cha ku Chigwa ndi kuyenda
kupita ku Chitsime cha Chirombo Cham'madzi mpaka ku Chipata cha
Zinyalala. Ndinayang'ana makoma a Yerusalemu, amene anagwetsedwa,
ndi zipata zake, zimene zinawonongedwa ndi moto. 14 Kenaka ndinapita
ku Chipata cha Kasupe ndi ku Dziwe la Mfumu. Koma panalibe malo ok-
wanira akuti bulu wanga adutse. 15 Kotero usikuwo ndinapita ku chigwa,
ndikuyang'ana khomalo. Pomaliza ndinabwerera ndi kukalowanso mu
mzinda kudzera ku Chipata cha ku Chigwa. 16 Akuluakulu sanadziwe
kumene ndinapita kapena zimene ndimachita, chifukwa pa nthawiyi
n'kuti ndisananene kalikonse kwa Ayuda kapena ansembe, anthu ole-
mekezeka kapena akuluakulu, kapena wina aliyense amene anali woyen-
era kugwira ntchitoyi.

17 Ndinawawuza kuti, "Inu mukuona mavuto amene tili nawo. Mukuona
kuti mzinda wa Yerusalemu wasanduka bwinja ndipo zipata zake zaten-
thedwa ndi moto. Tsono tiyeni timangenso makoma a Yerusalemu ndipo
sitidzachitanso manyazi." 18 Ndinawawuza za mmene Yehova Mulungu
wanga anandichitira zabwino ndiponso mawu amene mfumu inandiwuza.

Tsono anati, "Tiyeni tiyambenso kumanga." Kotero analimbitsana
mtima kuti ayambenso ntchito yabwinoyi.

[19] Koma Sanibalati wa ku Horoni, Tobiya wa ku Amoni ndi Gesemu Mwarabu atamva zimenezi, anatiseka ndi kutinyoza. Iwo anafunsa kuti, "Kodi muti ndi chiyani chimene mukuchitachi? Kodi mufuna kuwukira mfumu?"

[20] Koma ndinawayankha kuti, "Mulungu Wakumwamba atithandiza kuti zinthu zitiyendere bwino. Ife antchito ake tiyambapo kumanga. Koma inu mulibe gawo lanu muno mu Yerusalemu. Mulibe chokuyenerezani kulandira malo ano. Mulibenso chilichonse muno chokumbutsa za inu."

# 3

### *Anthu Omanga Makoma a Yerusalemu*

[1] Pambuyo pake Eliyasibu mkulu wa ansembe ndi ansembe anzake anayamba kugwira ntchito ndipo anamanganso Chipata cha Nkhosa. Iwo anachipatulira Mulungu ndipo anayika zitseko zake. Khoma limene analipatula linafika mpaka pa Nsanja ya Zana ndi Nsanja ya Hananeli.
[2] Anthu a ku Yeriko anamanga chigawo china pambali pake ndipo Zakuri mwana wa Imuri anamanga chigawo chinanso choyandikana nawo.

[3] Chipata cha Nsomba chinamangidwanso ndi ana a fuko la Hasena. Iwo anayika mitanda yake ndi zitseko, zotsekera zake, ndi mipiringidzo
yake. [4] Meremoti mwana wa Uriya, mwana wa Hakozi, anakonza chigawo choyandikana nacho. Motsatana naye, Mesulamu mwana wa Berekiya, mwana wa Mesezabeli anakonza chigawo china. Pambali pake, Zadoki
mwana wa Baana anakonzanso chigawo china. [5] Pambali pa iwowa anthu
a ku Tekowa anakonza chigawo china. Koma wolemekezeka awo anakana kugwira ntchito imene akuluakulu awo anawapatsa.

[6] Chipata cha Yesana chinakonzedwa ndi Yoyada mwana wa Paseya ndi Mesulamu mwana wa Besodeya. Iwo anayika mitanda yake ndi kuyika
zitseko, zotsekera zake ndi mipiringidzo yake. [7] Pambali pawo Melatiya
Mgibeyoni ndi Yadoni Mmerenoti ndiponso anthu a ku Gibiyoni ndi a ku Mizipa anakonza chigawo chawo mpaka ku nyumba ya bwanamkubwa
wa chigawo cha Patsidya pa Yufurate. [8] Pambali pawo Uzieli mwana
wa Harihaya wa m'gulu amisiri osula golide anakonzanso chigawo china. Pambali pake Hananiya mmodzi mwa anthu oyenga mafuta onunkhira, anakonzanso chigawo china. Iwo anakonzanso Yerusalemu
mpaka ku Khoma Lotambasuka. [9] Refaya mwana wa Huri wolamulira
theka la chigawo cha Yerusalemu anakonza chigawo china motsatana
nawo. [10] Kulumikiza ichi, Yedaya mwana wa Harumafi anakonza chigawo choyang'anana ndi nyumba yake, ndipo Hatusi mwana wa Hasabaneya
anakonzanso motsatana naye. [11] Malikiya mwana wa Harimu ndi Hasubu
mwana wa Pahati-Mowabu anakonzanso chigawo china ndiponso Nsanja
ya Ng'anjo. [12] Salumu mwana wa Halohesi wolamulira theka la chigawo
cha Yerusalemu, anakonzanso chigawo chotsatana nawo mothandizidwa ndi ana ake akazi.

[13] Chipata cha ku chigwa chinakonzedwa ndi Hanuni ndi anthu okhala ku Zanowa. Iwo anachimanganso ndi kuyika zitseko zake ndi zotsekera ndi mipiringidzo yake. Iwo anakonzanso khoma lotalika mamita 450 mpaka ku Chipata cha Zinyalala.

[14] Chipata cha Zinyalala chinakonzedwa ndi Malikiya mwana wa
Rekabu, wolamulira chigawo cha Beti-Hakeremu. Iye anachimanganso
ndi kuyika zitseko zake, zotsekera zake ndi mipiringidzo.

[15] Chipata cha Kasupe chinakonzedwa ndi Saluni mwana wa Koli-Hoze,
wolamulira chigawo cha Mizipa. Iye anachimanganso ndi kuyikanso
denga ndiponso zitseko, zotsekera ndi mipiringidzo yake. Iye anakonzanso
khoma la Dziwe la Siloamu limene lili pafupi ndi munda wa mfumu mpaka
ku makwerero otsikira potuluka mzinda wa Davide. [16] Pambali pa iyeyo,
Nehemiya mwana wa Azibuki, wolamulira theka la chigawo cha Beti Zuri
anakonza chigawo china mpaka kumalo oyang'anana ndi manda a Davide,
mpaka ku dziwe lokumba ndi ku nyumba ya anthu ankhondo.
[17] Pambali pake Alevi anakonza chigawo china, ndipo mtsogoleri wawo
anali Rehumi mwana wa Bani. Pambali pa iye Hasabiya wolamulira theka
la chigawo cha Keyila anagwira ntchito ku chigawo chake. [18] Pambuyo
pa iyeyu abale awo anapitiriza kukonza, ndipo mtsogoleri wawo anali
Bawai mwana wa Henadadi, wolamulira theka lina la chigawo cha Keyila.
[19] Motsatana naye Ezeri mwana wa Yesuwa, wolamulira Mizipa anakonza
chigawo chinanso choyang'anana ndi chikweza chofikira ku nyumba
yosungira zida za nkhondo pa ngodya. [20] Motsatana naye, Baruki mwana
wa Zakai anakonzanso chigawo china kuchokera pa ngodya mpaka pa
chitseko cha nyumba ya Eliyasibu mkulu wa ansembe. [21] Motsatana naye,
Meremoti mwana wa Uriya, mwana wa Hakozi anakonzanso chigawo
china kuchokera ku chitseko cha nyumba ya Eliyasibu mpaka kumapeto
kwake.
[22] Pambuyo pake ansembe okhala ku chidikha anakonzanso chigawo
china. [23] Pambuyo pawo, Benjamini ndi Hasubu anakonza kutsogolo
kwa nyumba zawo. Ndipo motsatana nawo, Azariya mwana wa Maaseya
mwana wa Ananiya, anakonza chigawo choyang'anana ndi nyumba zawo.
[24] Motsatana naye, Binuyi mwana wa Henadadi anakonzanso chigawo
china, kuchokera pa nyumba ya Azariya kukafika potsirizira pa ngodya.
[25] Palali mwana Uzai anakonza chigawo china choyang'anana ndi ngodya
ndi nsanja yotuluka pa nyumba yapamwamba ya mfumu ku bwalo la
alonda. Motsatana naye, Pedaya mwana wa Parosi, [26] ndi otumikira
m'Nyumba ya Mulungu amene amakhala pa khoma la Ofeli anakonza
chigawo china mpaka pa malo oyang'anana ndi Chipata cha Madzi kuloza
kummawa ndiponso nsanja yayitali ija. [27] Motsatana nawo, anthu a
ku Tekowa anakonzanso chigawo china choyang'anana ndi nsanja ija
yayikulu ndi yayitali mpaka ku khoma la Ofeli.

[28] Kuyambira ku Chipata cha Akavalo anakonza ndi ansembe ena ndipo
aliyense amakonza khoma loyang'anana ndi nyumba yake. [29] Motsatana
nawo, Zadoki mwana wa Imeri anakonza chigawo china choyang'anana
ndi nyumba yake. Motsatana naye, Semeya mwana wa Sekaniya, mlonda
wa Chipata cha Kummawa, anakonzanso khoma. [30] Hananiya mwana
wa Selemiya ndiponso Hanuni mwana wachisanu ndi chimodzi wa Zalafi
anakonza chigawo china. Motsatana naye, Mesulamu mwana wa Berekiya
anakonza chigawo choyang'anana ndi chipinda chake. [31] Motsatana naye,
Malikiya mmodzi mwa amisiri a golide anakonza chigawo china mpaka
ku nyumba ya atumiki a ku Nyumba ya Mulungu ndiponso ku nyumba
ya anthu amalonda moyang'anana ndi chipata cha Mifikade ndiponso

mpaka pa chipinda chapamwamba chapangodya. 32 Ndipo pakati pa
chipinda chapamwamba chapangodya ndi Chipata cha Nkhosa anakonza
ndi amisiri a golide ndi anthu amalonda.

# 4

*Adani a Nehemiya pa Ntchito Yake*

1 Sanibalati atamva kuti tikumanganso khoma anapsa mtima nayamba
kuseka ndi kunyogodola Ayuda kwambiri. 2 Ndipo anayankhula pamaso
pa abale ake ndi asilikali a Samariya kuti, “Kodi Ayuda ofowokawa
akuchita chiyani? Kodi iwo n’kumanganso khoma? Kodi adzaperekanso
nsembe? Kodi adzatsiriza ntchitoyi tsiku limodzi? Kodi adzachita kutenga
miyala yakale ija ndi mmene inapseramo?”

3 Tobiya wa ku Amoni, amene anali naye anati, “Chimene akumangacho
ngati nkhandwe itakwerapo, itha kugwetsa khoma lawolo!”

4 Tsono ndinayamba kupemphera kuti, “Timvereni, Inu Mulungu wathu,
mmene akutinyozera. Mulole kuti mawu awo onyoza awabwerere,
ndipo atengedwe ukapolo ku dziko lachilendo. 5 Musawakhululukire
mphulupulu zawo kapena kufafaniza machimo awo pamaso panu popeza
aputa ukali wanu pamaso pa anthu omanga khoma.”

6 Choncho ife tinamangabe khomalo kufikira lonse litafika theka la
msinkhu wake, chifukwa chakuti anthu anagwira ntchitoyo ndi mtima
wawo wonse.

7 Koma pamene Sanibalati, Tobiya, Aarabu, Aamoni ndi anthu a ku Asi-
dodi anamva kuti ntchito yokonzanso makoma a Yerusalemu ikupitirirabe
ndipo kuti mipata ikutsekedwa, anapsa mtima kwambiri. 8 Tsono onse
anapangana za chiwembu kuti abwere ndi kudzathira nkhondo anthu
a ku Yerusalemu ndi kuyambitsa mapokoso pakati pawo. 9 Koma ife
tinapemphera kwa Mulungu wathu ndipo tinayika alonda otiteteza kwa
adaniwo usiku ndi usana.

10 Pa nthawi yomweyi anthu a ku Yuda anati, “Mphamvu za anthu
onyamula zinyalala zikutha ndipo pali zinyalala zambiri. Choncho ife
sititha kumanga khomali.”

11 Adani athunso anati, “Iwo asanadziwe izi, kapena kutiona, tidzakhala
tili pakati pawo ndipo tidzawapha ndi kuyimitsa ntchitoyo.”

12 Ndipo Ayuda amene ankhala pafupi ndi adani athuwo anabwera
kakhumi konse kuchokera konse kumene ankakhala kudzatiwuza kuti
tibwereko ku ntchito.

13 Choncho kumbuyo kwa khoma, cha m’munsi mwake komanso
malo amene anali asanathe ndinayikamo anthu m’mabanja atatenga
malupanga, mikondo ndi mauta awo. 14 Popeza anthu ankachita mantha,
tsono ndinawawuza anthu olemekezeka, akuluakulu ndiponso anthu onse
kuti, “Musawaope. Kumbukirani kuti Ambuye ndi wamkulu ndipo ndi
woopsa. Choncho menyerani nkhondo abale anu, ana aamuna ndi aakazi,
akazi anu ndi nyumba zanu.”

15 Adani athu atamva kuti ife tadziwa za chiwembu chawo, anadziwanso
kuti Yehova walepheretsa zimene ankafuna kutichita. Choncho tinabwer-
era aliyense ku ntchito yake yomanga khoma.

16 Kuyambira tsiku limenelo mpaka m’tsogolo mwake, theka la antchito
anga linkagwira ntchito, pamene theka linalo limatenga mikondo, zis-
hango, mauta ndi kuvala malaya azitsulo. Akuluakulu ankalimbikitsa

Ayuda onse [17] amene ankamanga khoma. Anthu onyamula zinyalala aja
ankagwira ntchito ndi dzanja limodzi, dzanja linali atanyamula chida
chankhondo. [18] M'misiri aliyense ankamangirira lupanga lake m'chiwuno
mwake akamagwira ntchito. Koma munthu woyimba lipenga anali
pambali panga nthawi zonse.

[19] Ndipo ine ndinati kwa anthu olemekezeka ndi anthu ena onse,
"Ntchitoyi ndi yayikulu ndipo ili padera lalikulu ndipo ifeyo takhala
motayanatayana kwambiri pa khoma. [20] Tsono kulikonse kumene muliko,
mukamva kulira kwa lipenga bwerani mudzasonkhane kumene kuli ine
kuno. Mulungu wathu adzatimenyera nkhondo."

[21] Choncho enafe tinapitiriza kugwira ntchito, pamene theka lina
linkanyamula mikondo kuyambira m'bandakucha mpaka nyenyezi zi-
taoneka. [22] Pa nthawi imeneyo ndinawuzanso anthuwo kuti, "Aliyense
pamodzi ndi wantchito wake agone mu Yerusalemu kuti tikhale ndi
otilondera usiku ndi kuti masana tizigwira ntchito." [23] Choncho ine,
anzanga, antchito anga, ndi anthu otiteteza amene ankanditsata panalibe
ndi mmodzi yemwe anavula zovala zake pogona. Aliyense anasunga chida
chake chankhondo pambali pake.

# 5

## *Nehemiya Ateteza Anthu Aumphawi*

[1] Tsono anthu ena ndi akazi awo anayamba kudandaula kwambiri
chifukwa cha Ayuda anzawo. [2] Ena ankanena kuti, "Ife ndi ana athu
aamuna ndi aakazi, tilipo ochuluka kwambiri. Choncho tikufuna tirigu
kuti tidye ndi kukhala ndi moyo."

[3] Panali ena amene ankanena kuti, "Ife tikuchita kupereka minda yathu,
mitengo yathu ya mphesa ndi nyumba zathu ngati chikole kuti tipeze tirigu
chifukwa njala yakula."

[4] Panalinso ena amene ankanena kuti, "ife tinachita kukongola ndalama
zoti tipereke msonkho wa minda ndi mitengo yathu ya mphesa kwa
mfumu. [5] Ngakhale kuti ndife amodzi ndi abale athuwa, ndipo
ngakhalenso ana athu ndi ofanana ndi ana awo, ife tikukakamiza ana athu
kuti akhale akapolo. Ena mwa ana athu aakazi atengedwa kale ukapolo.
Ife tilibe mphamvu yochitapo kanthu popeza anthu ena anatenga kale
minda yathu ndi mitengo yathu ya mphesa."

[6] Nditamva madandawulo awo ndi zimene amanenazi ndinapsa mtima
kwambiri. [7] Nditalingalira bwino ndinatsimikiza zoti ndichitepo kan-
thu ndipo kenaka ndinawadzudzula anthu olemekezeka ndi akuluaku-
luwo. Ndinawawuza kuti, "Zoona ndithu inu n'kumalipiritsana chi-
wongoladzanja chachikulu anthu apachibale nokhanokha!" Choncho
ndinayitanitsa msonkhano waukulu kuti ndiwazenge mlandu [8] ndipo
ndinati, "Monga zakhaliramu ife tikutha kuwombola abale anthu amene
anagulitsidwa ukapolo kwa anthu ena. Kodi tsopano inu mukugulitsanso
abale anu kwa anzawo kuti ife tiwumirizidwe kuwawombola?" Iwo
anakhala chete, chifukwa sanapeze mawu oti anene.

[9] Kotero ndinapitiriza kunena kuti, "Zimene mukuchitazi si zabwino.
Kodi inu simungakhale ndi moyo woopa Mulungu wathu kuti tipewe
kunyoza kwa adani athu, anthu a mitunda inayi? [10] Ine ndi abale
anga ndiponso antchito anga tikuwakongozanso anthuwa ndalama ndi
tirigu. Ndipo tiyeni tilekeretu zolandira chiwongoladzanja! [11] Abwezereni
lero lomwe minda yawo, mitengo ya mphesa, mitengo ya olivi ndiponso

nyumba zawo. Muwabwezerenso chiwongoladzanja cha ndalama, tirigu,
vinyo ndi mafuta zimene munatenga.”

12 Iwo anayankha kuti, “Ife tidzawabwezera zimenezi popanda kupem-
phapo kanthu kalikonse kwa iwo. Tidzachita monga mwanena.”

Pambuyo pake ndinayitanitsa ansembe ndipo pamaso pawo ndi-
nawalumbiritsa atsogoleriwo ndi akuluakuluwo kuti adzachitadi zomwe
analonjezazo. 13 Ndipo inenso ndinakutumula chovala changa ndi
kuti, “Chimodzimodzinso Mulungu akutumule munthu wosasunga malon-
jezano ake. Amulande nyumba yake ndi katundu wake ndi kumusandutsa
m’mphawi!”

Apo msonkhano wonse unati, “Ameni” natamanda Yehova. Ndipo anthu
aja anachita monga analonjezera.

14 Ndiponso kuyambira nthawi imene anandisankha kuti ndikhale
bwanamkubwa wa dziko la Yuda, kuchokera chaka cha makumi awiri
mpaka chaka cha 32 muulamuliro wa ufumu wa Aritasasita, ndiye kuti
kwa zaka zokwana 12, ine ngakhale abale anga sitinalandire chakudya
choyenerera bwanamkubwa. 15 Koma abwanamkubwa akale ankasautsa
anthu. Iwo ankalanda anthu chakudya ndi vinyo ndi kuwalipiritsanso
masekeli asiliva makumi anayi. Ngakhalenso antchito awo amavutitsa
anthu kwambiri. Koma ine sindinachite zimenezo chifukwa ndimaopa
Mulungu. 16 Ndiponso ndinadzipereka kugwira ntchito yomanga khoma
la mzinda wa Yerusalemu popanda ngakhale kugulapo munda. Antchito
anganso anasonkhana komweko kuti agwire ntchito ndipo sitinafunenso
malo ena.

17 Kuwonjezera apa, ndinkadyetsa Ayuda, akuluakulu kuphatikizanso
anthu amene ankabwera kwa ife kuchokera kwa mitundu ya anthu
otizungulira okwanira 150. 18 Tsiku lililonse pamaphikidwa ng’ombe
imodzi, nkhosa zabwino zisanu ndi imodzi pamodzi ndi nkhuku. Ndipo
pakutha pa masiku khumi aliwonse pankakhala matumba achikopa
ochuluka a vinyo wa mitundu yonse. Ngakhale zinali choncho, Ine
sindinatenge chakudya choperekedwa kwa bwanamkubwa, chifukwa izi
zinali zosautsa anthu.

19 Kuti zinthu zindiyendere bwino, kumbukirani Yehova Mulungu
wanga pa zonse zimene ndachitira anthu awa.

# 6

### *Adani Apitiriza Kutsutsa ndi Kuopseza Nehemiya*

1 Pamenepo Sanibalati, Tobiya, Gesemu Mwarabu ndi adani athu
anamva kuti ndatsiriza ntchito yomanganso khoma ndi kuti palibe mpata
umene watsala ngakhale kuti pa nthawi imeneyi ndinali ndisanayike
zitseko pa zipata. 2 Sanibalati ndi Gesemu, ananditumizira uthenga uwu:
“Bwerani tidzakumane pa mudzi wina ku chigwa cha Ono.”

Koma iwo anakonzekera kuti akandichite chiwembu kumeneko.
3 Choncho ine ndinatuma amithenga ndi yankho ili: “Ine ndikugwira
ntchito yayikulu kuno ndipo sindingathe kubwera kumeneko. Kodi ntchito
iyime pofuna kuti ndibwere kumeneko?” 4 Ananditumizira uthenga
umodzimodzi omwewu kanayi ndipo ndinawayankha chimodzimodzi.

5 Tsono kachisanu, Sanibalati anatumiza wantchito wake ndi kalata
yosamata. 6 Mu kalatamo munali mawu akuti,

> “Pali mphekesera pakati pa mitundu ya anthu, ndiponso Gesemu
> akunena zomwezo kuti inu ndi Ayuda onse mufuna kuwukira boma.
> N’chifukwa chake mukumanga khoma. Mphekeserazo zikutinso inu

mukufuna kudzakhala mfumu yawo. 7 Mwayikanso kale aneneri amene
adzalengeza za iwe mu Yerusalemu kuti 'Mu Yuda muli mfumu!'
Tsono nkhani iyi imveka ndithu kwa mfumu. Choncho bwerani kuti
tidzakambirane."

8 Ine ndinatumiza yankho ili: "Pa zimene mukunenazo, palibe chimene
chinachitikapo. Inu mukungozipeka m'mutu mwanu."

9 Apa adani athu onsewa ankangofuna kutiopseza. Iwo ankaganiza kuti
"Tichita mantha ndi kuleka kugwira ntchito."

Tsono ndinapemphera kuti, "Inu Mulungu ndilimbitseni mtima."

10 Tsiku lina ndinapita ku nyumba ya Semaya mwana wa Delaya
mwana wa Mehatabeli. Tsono anandiwuza kuti, "Tiyeni tikakumanire ku
Nyumba ya Mulungu. Tikabisale m'menemo ndi kutseka zitseko chifukwa
akubwera kudzakuphani. Ndithu usiku uno akubwera kudzakuphani."

11 Koma ndinayankha kuti, "Kodi munthu ngati ine n'kuthawa?
Kapena munthu wofanana ndi ine n'kupita ku Nyumba ya Mulungu
kuti apulumutse moyo wake? Ayi, ine sindipita!" 12 Ndinazindikira
kuti Mulungu sanamutume koma kuti anayankhula mawu oloserawa
motsutsana nane chifukwa Tobiya ndi Sanibalati anamulemba ntchitoyi.
13 Iye analembedwa ntchitoyi ndi cholinga choti ine ndichite mantha,
ndithawe. Ndikanatero ndiye kuti ndikanachimwira Yehova ndiponso
iwowo akanandiyipitsira mbiri yanga ndi kumandinyoza.

14 Tsono ndinapemphera kuti, "Inu Mulungu wanga, kumbukirani To-
biya ndi Sanibalati chifukwa cha zimene achita. Kumbukiraninso mneneri
wamkazi Nowadiya ndi aneneri amene akhala akufuna kundiopseza."

### *Kutsiriza kwa Khoma*

15 Ndipo khoma linatsirizidwa kumanga pa tsiku la 25 la mwezi wa
Eluli. Linamangidwa pa masiku okwana 52. 16 Adani athu onse atamva
izi, mitundu yonse ya anthu yozungulira inachita mantha ndi kuchita
manyazi. Iwo anazindikira kuti ntchitoyo inachitika ndi thandizo la
Mulungu wathu.

17 Komanso masiku amenewo anthu olemekezeka a ku Yuda ankalem-
berana naye makalata ambiri ndi Tobiyayo, 18 pakuti anthu ambiri a ku
Yuda anali atalumbira kale kuti adzagwira naye ntchito popeza anali
mkamwini wa Sekaniya mwana wa Ara, ndipo mwana wake Yeho-
hanani anakwatira mwana wamkazi wa Mesulamu mwana wa Berekiya.
19 Kuwonjezera apo, anthu ankasimba za ntchito zake zabwino ine
ndili pomwepo ndipo anakamuwululira mawu anga. Choncho Tobiyayo
ankatumiza makalata ondiopseza.

## 7

1 Khoma linamangidwa ndipo zitseko zinayikidwa. Pambuyo pake
alonda a Nyumba ya Mulungu, oyimba nyimbo ndiponso Alevi
anasankhidwa. 2 Kenaka ine ndinasankha m'bale wanga Hanani
pamodzi ndi Hananiya woyang'anira nsanja yankhondo kukhala ola-
mulira Yerusalemu chifukwa iyeyu anali munthu odalirika ndi woopa
Mulungu kuposa anthu ena. 3 Ine ndinawawuza kuti, "Musalole kuti
zipata za Yerusalemu zitsekulidwe mpaka dzuwa litatentha, ndipo alonda
asanaweruke aonetsetse kuti atseka zitseko ndi kuzipiringidza. Musankhe
alonda pakati pa anthu okhala mu Yerusalemu, ena akhale pa malo pawo
ndi ena akhale moyang'anana ndi nyumba zawo."

### *Mndandanda wa Anthu Oyamba Kubwera Kuchokera ku Ukapolo*

4 Tsono mzinda wa Yerusalemu unali wotambasuka ndiponso waukulu
koma munali anthu ochepa ndipo nyumba zinali zisanamangidwe. 5 Ndipo
Mulungu wanga anayika mu mtima mwanga maganizo oti ndisonkhanitse
anthu olemekezeka, akuluakulu ndi anthu onse kuti alembetse mayina
mwa mabanja awo. Ndinapeza buku limene munalembedwa mayina a
mabanja a iwo amene anayamba kubwera kuchokera ku ukapolo. Izi ndi
zimene ndinazipeza zitalembedwa m'menemo:

6 Awa ndi anthu a m'chigawo cha Yuda amene anabwerera kuchokera
ku ukapolo amene Nebukadinezara mfumu ya Babuloni anawatenga
ukapolo. Iwo anabwerera ku Yerusalemu ndi ku Yuda, aliyense ku
mzinda wa makolo ake. 7 Anabwera pamodzi ndi atsogoleri awa:
Zerubabeli, Yesuwa, Nehemiya, Azariya, Raamiya, Nahamani, Mordekai,
Bilisani, Misipereti, Bigivai, Nehumu ndi Baana.

Tsono chiwerengero cha anthu a ku Israeli chinali chotere:

| |
|---|
| 8 Zidzukulu za Parosi |
| 9 Zidzukulu za Sefatiya |
| 10 Zidzukulu za Ara |
| 11 Zidzukulu za Pahati-Mowabu (kudzera mu m'bado wa Yesuwa ndi Yowabu) |
| 12 Zidzukulu za Elamu |
| 13 Zidzukulu za Zatu |
| 14 Zidzukulu za Zakai |
| 15 Zidzukulu za Binuyi |
| 16 Zidzukulu za Bebai |
| 17 Zidzukulu za Azigadi |
| 18 Zidzukulu za Adonikamu |
| 19 Zidzukulu za Abigivai |
| 20 Zidzukulu za Adini |
| 21 Zidzukulu za Ateri (kudzera mwa Hezekiya) |
| 22 Zidzukulu za Hasumu |
| 23 Zidzukulu za Bezayi |
| 24 Zidzukulu za Harifu |
| 25 Zidzukulu za Gibiyoni |

| | |
|---|---|
| 26 Anthu a ku Betelehemu ndi Netofa | 188 |
| 27 Anthu a ku Anatoti | 128 |
| 28 Anthu a ku Beti-Azimaveti | 42 |
| 29 Anthu a ku Kiriati Yeyarimu Kefira ndi Beeroti | 743 |
| 30 Anthu a ku Rama ndi Geba | 621 |
| 31 Anthu a ku Mikimasi | 122 |
| 32 Anthu a ku Beteli ndi Ai | 123 |
| 33 Anthu a ku Nebo winayo | 52 |
| 34 Ana a Elamu wina | 1,254 |
| 35 Zidzukulu za Harimu | 320 |
| 36 Zidzukulu za Yeriko | 345 |
| 37 Zidzukulu za Lodi, Hadidi ndi Ono | 721 |
| 38 Zidzukulu za Senaya | 3,930. |

39 Ansembe anali awa:

| | |
|---|---|
| A banja la Yedaya (ndiye kuti zidzukulu za Yesuwa) | 973 |
| 40 Zidzukulu za Imeri | 1,052 |
| 41 Zidzukulu za Pasi-Huri | 1,247 |
| 42 Zidzukulu za Harimu | 1,017. |

43 Alevi anali awa:

| | |
|---|---|
| A banja la Yesuwa ndi Kadimieli, ndiye kuti zidzukulu za Hodaviya | 74. |

44 Anthu oyimba:

| | |
|---|---|
| Zidzukulu za Asafu | 148. |

45 Alonda a ku Nyumba ya Mulungu anali awa:

| | |
|---|---|
| Zidzukulu za | |
| Salumu, Ateri, Talimoni, Hatita ndi Sobai | 138. |

46 Anthu ogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu anali awa:

| |
|---|
| Zidzukulu za |
| Ziha, zidzukulu za Hasufa, zidzukulu za Tabaoti, |
| 47 Zidzukulu Kerosi, zidzukulu za Siya, zidzukulu za Padoni |
| 48 Zidzukulu za Lebana za Hagaba, ndi za Salimayi, |
| 49 Zidzukulu za Hanani, zidzukulu za Gideli, zidzukulu za Gahari, |
| 50 Zidzukulu za Reyaya, zidzukulu za Rezini, zidzukulu za Nehoda, |
| 51 Zidzukulu za Gazamu, zidzukulu za Uza, zidzukulu za Paseya, |
| 52 Zidzukulu za Besai, zidzukulu za Meunimu, zidzukulu za Nefusimu, |
| 53 Zidzukulu za Bakibuku, zidzukulu za Hakufa, zidzukulu za Harihuri, |
| 54 Zidzukulu za Baziliti, zidzukulu za Mehida, zidzukulu za Harisa, |
| 55 Zidzukulu za Barikosi, zidzukulu za Sisera, zidzukulu za Tema |
| 56 Zidzukulu za Neziya, ndi zidzukulu za Hatifa. |

57 Zidzukulu za antchito a Solomoni:

| |
|---|
| Zidzukulu za |
| Sotai, zidzukulu za Sofereti, zidzukulu za Perida |
| 58 zidzukulu za Yaala, zidzukulu za Darikoni, zidzukulu za Gideli, |
| 59 zidzukulu za Sefatiya, zidzukulu za Hatilu |
| zidzukulu za Pokereti-Hazebaimu ndi zidzukulu Amoni. |
| 60 Anthu onse ogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu pamodzi ndi zidzukulu z |

61 Ali munsiwa anachokera ku Teli-Mela, Teri-Harisa, Kerubi, Adoni, ndi Imeri, koma sanathe kunena mwa tchutchutchu kuti makolo awo kapena mafuko awo analidi Aisraeli kapena ayi.

| | |
|---|---|
| 62 Zidzukulu za | |
| Delaya, zidzukulu za Tobiya ndi zidzukulu za Nekoda | 642. |

63 Ndiponso ena pakati pa ansembe anali awa:
zidzukulu za
Hobiya, zidzukulu za Hakozi ndi zidzukulu za Barizilai (munthu amene anakwatira mwana wamkazi wa Barizilai wa ku Giliyadi ndipo amatchedwa dzina limenelo).
64 Iwowa anafufuzafufuza mayina awo m'buku la mibado ya mabanja awo ndipo sanapeze mayina awo kotero anachotsedwa pa
unsembe nawerengedwa ngati odetsedwa pa chipembedzo. 65 Choncho
bwanamkubwa anawawuza anthuwo kuti asamadye nawo chakudya china chilichonse choperekedwa kwa Mulungu mpaka patapezeka wansembe wodziwa kugwiritsa bwino ntchito ya Urimu ndi Tumimu.

66 Chiwerengero chonse cha anthuwa chinali 42,360. 67 Kuwonjezera
pamenepa panali antchito awo aamuna ndi aakazi 7,337 ndiponso anthu
aamuna ndi aakazi oyimba nyimbo okwanira 245. 68 Panali akavalo 736,
abulu ang'onoang'ono 245. 69 Ngamira zawo zinalipo 435 ndipo abulu
analipo 6,720.

70 Atsogoleri ena a mabanja anapereka mphatso zothandizira ntchito.
Bwanamkubwa anapereka ku thumba losungira chuma, ndalama
zagolide za makilogalamu asanu ndi atatu, mabeseni makumi asanu
ndi zovala za ansembe 530. 71 Atsogoleri ena amabanja anapereka ku
thumba losungira chuma ndalama zagolide zokwana makilogalamu 168,
ndiponso ndalama za siliva zokwana makilogalamu 1,250. 72 Anthu
ena onse otsala anapereka ndalama zagolide zokwana makilogalamu
168, ndalama za siliva zokwana makilogalamu 140, ndiponso zovala za
ansembe 67.
73 Choncho ansembe, Alevi, alonda a Nyumba ya Mulungu, anthu oyimba
nyimbo, ena mwa anthu wamba, ogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu
pamodzi ndi Aisraeli ena onse ankakhala m'mizinda yawo.

*Ezara Awerenga Malamulo*

Pofika mwezi wachisanu ndi chiwiri Aisraeli onse anali atakhazikika m'mizinda yawo.

## 8

1 Anthu onse anasonkhana ngati munthu mmodzi pabwalo limene lili
patsogolo pa Chipata cha Madzi. Iwo anawuza mlembi Ezara kuti abwere
ndi buku la malamulo a Mose limene Yehova anapereka kwa Aisraeli.

2 Choncho pa tsiku loyamba la mwezi wachisanu ndi chiwiri wansembe
Ezara, anabwera ndi buku la malamulo ku msonkhano wa amuna, akazi
ndi ana onse amene ankatha kumvetsa zinthu bwino. 3 Choncho Ezara
anawerenga bukulo atayang'ana bwalo la Chipata cha Madzi kuyambira
mmawa mpaka masana pamaso pa amuna, akazi ndi onse amene
ankamvetsa bwino zinthu. Ndipo anthu onse anatchera khutu kuti amve
malamulowo.

4 Mlembi Ezara anayimirira pa nsanja ya mitengo imene anthu anamanga chifukwa cha msonkhanowu. Ku dzanja lake lamanja kunayimirira Matitiya, Sema, Anaya, Uriya, Hilikiya ndi Maaseya, ndipo kudzanja lake lamanzere kunali Pedaya, Misaeli, Malikiya, Hasumu, Hasibadana, Zekariya ndi Mesulamu.

5 Tsono Ezara anatsekula buku, akuona popeza anayima pa nsanja.
Pamene anafutukula bukulo anthu onse anayimirira. 6 Ezara anatamanda
Yehova, Mulungu wamkulu, ndipo anthu onse anakweza manja awo ndi
kuyankha kuti, "Ameni, ameni." Pambuyo pake onse anaweramitsa pansi
mitu yawo napembedza Yehova akanali chizolikire choncho.

7 Anthuwo atayimiriranso Alevi awa: Yesuwa, Bani, Serebiya, Yamini,
Akubu, Sabetayi, Hodiya, Maaseya, Kerita, Azariya, Yozabadi, Hanani ndi
Pelaya anawathandiza kuti amvetse bwino malamulowo. 8 Iwo anaw-
erenga buku la malamulo a Mulungu momveka bwino ndi kutanthauzira
mawuwo kuti anthu amvetse bwino zowerengedwazo.

9 Tsono bwanamkubwa Nehemiya pamodzi ndi wansembe ndi mlembi Ezara komanso Alevi amene amaphunzitsa anthu anati kwa anthu onse, "Lero ndi tsiku lopatulika kwa Yehova Mulungu wanu. Musakhale ndi chisoni ndipo musalire." Anayankhula choncho popeza anthu onse ankalira atamva mawu a buku la malamulo lija.

10 Nehemiya anatinso, "Pitani, kachiteni phwando ku nyumba ndipo mukawagawireko ena amene alibe kanthu kalikonse popeza lero ndi tsiku lopatulika kwa Yehova. Musakhale ndi chisoni, pakuti chimwemwe cha Yehova ndiye mphamvu yanu."

11 Alevi anakhalitsa bata anthu onse powawuza kuti, "Khalani chete,
pakuti lero ndi tsiku lopatulika ndipo musakhale ndi chisoni."
12 Anthu onse anachoka kupita kukadya ndi kumwa. Chakudya china ana-
tumiza kwa anzawo. Choncho panali chikondwerero chachikulu popeza
tsopano anali atamvetsa bwino mawu a Mulungu amene anawawerengera
ndi kuwafotokozerawo.
13 Mmawa mwake atsogoleri a mabanja pamodzi ndi ansembe ndi
alevi anasonkhana kwa Ezara, mlembi wa malamulo kuti aphunzire
mawu a malamulowo. 14 Tsono anapeza kuti zinalembedwa m'buku
la malamulo kuti Yehova analamula kudzera mwa Mose kuti Aisraeli
azikhala m'zithando pa nthawi yonse ya chikondwerero cha mwezi
wachisanu ndi chiwiri. 15 Choncho analengeza ndi kufalitsa m'mizinda
yawo yonse ndi mu Yerusalemu kuti, "Pitani ku phiri mukadule nthambi
za mtengo wa olivi, za mtengo wa olivi wa kutchire, za mtengo wa
mchisu, za mtengo wa mgwalangwa ndiponso za mitengo ina ya masamba,
zomangira zithando monga zalembedweramu ndi kubwera nazo."
16 Choncho anthu anapita kukatenga nthambi ndipo aliyense anadziman-
gira misasa pa denga ya nyumba yake, m'mabwalo awo, m'mabwalo a
Nyumba ya Mulungu, m'bwalo la pa Chipata cha Madzi ndiponso m'bwalo
la pa Chipata cha Efereimu. 17 Gulu lonse la anthu limene linabwera
ku ukapolo linamanga misasa ndipo linakhala m'menemo. Kuyambira
nthawi ya Yoswa mwana wa Nuni mpaka tsiku limenelo n'kuti Aisraeli
asanachitepo zimenezi. Choncho panali chimwemwe chachikulu.
18 Tsiku ndi tsiku, kuyambira tsiku loyamba mpaka lomaliza, Ezara ankaw-
erenga buku la malamulo a Mulungu. Anthu anachita chikondwerero
masiku asanu ndi awiri. Pa tsiku lachisanu ndi chitatu panachitika
msonkhano potsata buku la malamulo lija.

# 9

## *Aisraeli Avomereza Kuchimwa Kwawo*

1 Pa tsiku la 24 la mwezi womwewo, Aisraeli anasonkhana pamodzi
ndi kusala chakudya, kuvala ziguduli ndi kudzithira dothi pa mutu.
2 Aisraeliwa anadzipatula pakati pa anthu a mitundu ina ndipo anay-
imirira nayamba kuwulula machimo awo ndi zolakwa za makolo awo.
3 Anthuwo anayimirira pomwepo, ndipo anamva mawu a m'buku la
malamulo a Yehova akuwerengedwa kwa maora enanso atatu ndipo
anakhala maora ena atatu akuwulula machimo awo ndi kupembedza
Yehova Mulungu wawo. 4 Pa makwerero okhalapo alevi anayimirirapo
anthu awa: Yesuwa, Bani, Kadimieli, Sebaniya, Buni, Serebiya, Bani ndi
Kenani. Iwowa ankapemphera mokweza mawu kwa Yehova Mulungu
wawo. 5 Ndipo Alevi awa: Yesuwa, Kadimieli, Bani, Hasabaneya, Serebiya,
Hodiya, Sebaniya ndi Petahiya anati: "Imirirani ndipo mutamande Yehova
Mulungu wanu, amene ndi wamuyaya."

"Litamandike dzina lake laulemerero limene liposa madalitso ndi
matamando onse. 6 Inu nokha ndiye Yehova. Munalenga
kumwamba, ngakhale kumwambamwamba, zolengedwa zonse zimene
zili m'menemo. Munalenga dziko ndi zonse zokhalamo, nyanja ndi
zonse zili m'menemo. Zonse mumazisunga ndi moyo ndipo zonse za
kumwamba zimakupembedzani.

7 "Inu ndinu Yehova Mulungu amene munasankha Abramu ndi kumutu-
lutsa m'dziko la Uri wa ku Kaldeya ndi kumutcha dzina lake Abrahamu.
8 Inu munaona kuti mtima wake unali wokhulupirika kwa inu, ndipo

munapangana naye pangano lakuti mudzapereka kwa zidzukulu zake
dziko la Akanaani Ahiti, Aamori, Aperezi, Ayebusi ndi Agirigasi. Inu
mwasunga lonjezo lanu chifukwa ndinu wolungama.
9 “Munaona kuzunzika kwa makolo athu ku Igupto. Munamva kufuwula
kwawo pa Nyanja Yofiira. 10 Inu munachita zizindikiro zozizwitsa ndi
zodabwitsa kutsutsana ndi Farao, pamaso pa Farao, nduna zake ndi
anthu onse a m'dziko lake, pakuti Inu munadziwa kuti anazunza makolo
athu. Inu munadzipangira nokha dzina, monga zilili mpaka lero lino.
11 Inu munagawa nyanja anthu anu akupenya, kotero kuti anadutsa
powuma, koma munamiza m'madzi akuya anthu amene ankawalondola
monga mmene uchitira mwala m'madzi ozama. 12 Masana munkawu-
nikira ndi chipilala cha mtambo ndipo usiku munkawunikira ndi
chipilala cha moto njira yonse imene ankayendamo.
13 “Munatsika pa Phiri la Sinai, ndipo munawayankhula kuchokera
kumwamba. Munawapatsa malangizo olungama, ziphunzitso zoona
ndiponso malamulo abwino. 14 Inu munawadziwitsa kuti tsiku lanu
la Sabata ndi loyera ndipo munawapatsa malamulo ndi ziphunzitso.
15 Pamene anali ndi njala munawapatsa buledi wochokera kumwamba.
Pamene anali ndi ludzu munawapatsa madzi otuluka m'thanthwe.
Munawawuza kuti apite kukalanda dziko limene munalonjeza kuti
mudzawapatsa.”
16 “Koma makolo athu anadzikuza ndi kuwumitsa khosi, ndipo iwo
sanamvere malamulo anu. 17 Anakana kumvera ndipo sanakumbukire
zodabwitsa zimene munachita pakati pawo. Koma iwo anawumitsa
khosi, nakuwukirani podzisankhira okha mtsogoleri kuti awatsogolere
kubwerera ku ukapolo ku dziko la Igupto. Koma ndinu Mulungu
wokhululukira, wokoma mtima ndi wachifundo wosapsa mtima msanga
ndi wachikondi chachikulu chosasinthika. Choncho Inu simunawasiye.
18 Ngakhale pamene iwo anadziwumbira fano la mwana wang'ombe ndi
kuti, ‘Uyu ndi mulungu wanu amene anakutulutsani m'dziko la Igupto,’
kapena pamene anachita chipongwe choopsa.
19 “Koma Inu ndi chifundo chanu chachikulu, simunawasiye m'chipululu.
Chipilala cha mtambo sichinasiye kuwatsogolera pa njira yawo masana
ndipo chipilala cha moto sichinasiye kuwatsogolera pa njira yawo usiku.
20 Inu munawapatsa mzimu wanu wabwino kuti uwalangize. Inu
simunawamane chakudya cha mana chija, ndipo munawapatsa madzi
akumwa. 21 Munawasunga zaka makumi anayi m'chipululu ndipo
sanasowe kanthu kalikonse. Zovala zawo sizinathe kapena mapazi awo
kutupa.”
22 “Inu munawapatsa mafumu ndi mayiko m'manja mwawo. Munawa-
gawiranso mayiko achilendo akutali kwambiri. Munabwera nawo
m'dziko la Sihoni mfumu ya Hesiboni ndi dziko la Ogi mfumu ya
Basani kuti alowemo n'kulitenga kukhala lawo. 23 Munachulukitsa ana
awo aamuna ngati nyenyezi za mlengalenga. Ndipo munawabweretsa
m'dziko limene munawuza makolo awo kuti alilowe ndi kulitenga.
24 Choncho zidzukulu zawo zinapita ndi kukalandira dzikolo. Inu
munagonjetsa pamaso pawo, Akanaani amene amakhala m'dzikolo.
Inde munapereka m'manja mwawo mafumu awo pamodzi ndi anthu
a m'dzikomo kuti achite nawo monga angafunire. 25 Iwo analanda
mizinda yotetezedwa ndi dziko lachonde. Anatenganso nyumba zodzaza
ndi zinthu zonse zabwino, zitsime zokumbidwa kale, mitengo ya
mphesa, mitengo ya olivi ndi mitengo yambiri ya zipatso. Ndipo anadya

nakhuta ndipo anali athanzi. Choncho ankakondwa chifukwa cha
ubwino wanu wopambana.
26 "Komabe iwo anakhala osamvera ndipo anakuwukirani nafulatira
malamulo anu. Anapha aneneri anu, amene anakawadandaulira
kuti abwerere kwa Inu. Anachita chipongwe choopsa. 27 Pamene
anazunzidwa anafuwulira kwa Inu, ndipo Inu munawamvera muli
kumwambako. Ndipo mwa chifundo chanu chachikulu munkawapatsa
atsogoleri amene ankawapulumutsa m'manja mwa adani awo."
28 "Koma akangokhala pa mtendere ankayambanso kuchita zoyipa pamaso
panu. Choncho munkawapereka m'manja mwa adani awo amene
ankawalamulira. Komabe pamene ankabwerera ndi kumalira kwa Inu,
Inu munkawamva muli kumwambako. Chifukwa cha chifundo chanu
chochuluka, nthawi zonse munkawapulumutsa.
29 "Inu munkawachenjeza kuti abwerere ndi kuyamba kutsata malamulo
anu. Koma iwo ankadzitukumula ndipo sankamvera malamulo anu.
Iwo anachimwira malangizo anu amene munati 'Amapatsa moyo
kwa munthu wowamvera.' Iwo ankakufulatirani, nawumitsa makosi
awo osafuna kukumverani. 30 Munapirira nawo kwa zaka zambiri.
Munkawachenjeza ndi Mzimu wanu kudzera mwa aneneri anu, koma
iwo sankakumverani. Choncho munawapereka m'manja mwa anthu a
mayiko ena. 31 Komabe mwachifundo chanu chachikulu simuwatheretu
kapena kuwataya pakuti ndinu Mulungu wokoma mtima ndi wachi-
fundo.
32 "N'chifukwa chake, tsono, Inu Mulungu wathu, Mulungu wamkulu,
wamphamvu ndi woopsa kwambiri mumasunga pangano ndi chikondi
chosasinthika. Musalole kuti mavuto onse amene atigwera ife, mafumu
athu, atsogoleri athu, ansembe athu, aneneri athu, makolo athu ndi
anthu ena onse kuyambira nthawi ya mafumu a ku Asiriya mpaka lero
aoneke ochepa pamaso panu. 33 Koma Inu mwakhala wolungama pa
zonse zimene zakhala zikutichitikira. Mwachita zokhulupirika, koma
ife tachita zolakwa. 34 Ndipotu mafumu athu, atsogoleri athu, ansembe
athu ndi makolo athu sanatsatire mawu anu. Iwo sanalabadire za
malamulo anu ngakhale mawu anu owachenjeza amene munawapatsa.
35 Ngakhale ankadzilamulira okha, n'kumalandira zabwino zochuluka
m'dziko lalikulu ndi lachonde limene munawapatsa, koma iwo sanaku-
tumikireni kapena kusiya ntchito zawo zoyipa.
36 "Tsono, taonani! Ife lero ndife akapolo, ndife akapolo m'dziko limene
munapereka kwa makolo athu kuti azidya zipatso zake ndi zabwino
zake zonse. 37 Tsono chifukwa cha machimo athu, mafumu amene
munawayika kuti azitilamulira angodzilemeretsa ndi chuma chambiri
cha dzikoli. Iwo ali ndi mphamvu zolamulira matupi athu ndi ng'ombe
zathu momwe afunira. Zedi, ife tili m'mavuto aakulu."

### *Mgwirizano wa Anthu*

38 "Chifukwa cha zonsezi, ife tikuchita mgwirizano wokhazikika, pochita
kulemba, ndipo atsogoleri athu, Alevi athu ndi ansembe athu asindikiza
chidindo chawo pa mgwirizanowo."

## 10

1 Amene anasindikiza chidindo anali awa:

Nehemiya, bwanamkubwa uja, mwana wa Hakaliya.

Zedekiya, 2 Seraya, Azariya, Yeremiya
3 Pasuri, Amariya, Malikiya,
4 Hatusi, Sebaniya, Maluki,
5 Harimu, Meremoti, Obadiya,
6 Danieli, Ginetoni, Baruki,
7 Mesulamu, Abiya, Miyamini
8 Maziya, Biligai ndi Semaya
Awa anali ansembe.

9 Alevi anali awa:
Yesuwa mwana wa Azaniya, Binuyi wa fuko la Henadadi, Kadimieli,
10 ndi abale awo awa: Sebaniya,
Hodiya, Kelita, Pelaya, Hanani,
11 Mika, Rehobu, Hasabiya,
12 Zakuri, Serebiya, Sebaniya,
13 Hodiya, Bani ndi Beninu.

14 Atsogoleri a anthu anali awa:
Parosi, Pahati-Mowabu, Elamu, Zatu, Bani,
15 Buni, Azigadi, Bebai,
16 Adoniya, Bigivai, Adini,
17 Ateri, Hezekiya, Azuri,
18 Hodiya, Hasumu, Bezayi
19 Harifu, Anatoti, Nebayi,
20 Magipiyasi, Mesulamu, Heziri
21 Mesezabeli, Zadoki, Yaduwa
22 Pelatiya, Hanani, Ananiya,
23 Hoseya, Hananiya, Hasubu
24 Halohesi, Piliha, Sobeki,
25 Rehumu, Hasabiya, Maaseya,
26 Ahiya, Hanani, Anani,
27 Maluki, Harimu ndi Baana.

28 Ife otsalafe, ndiye kuti ansembe, Alevi, alonda a ku Nyumba ya Mulungu, oyimba nyimbo, ogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu, onse amene anadzipatula pakati pa anthu a mitundu ina kuti atsate malamulo a Yehova, pamodzi ndi akazi athu, ana athu ndi onse amene ali ndi nzeru,
29 tikuphatikana ndi abale athu wolemekezeka, ndipo tikulonjeza molumbira kuti tidzayenda motsata malamulo a Mulungu amene anapereka kudzera mwa Mose mtumiki wa Mulungu. Tilonjeza kumvera ndi kutsata bwino mawu onse, miyambo yonse ndi malangizo onse a Yehova. Yehova atilange ngati sitidzachita zimenezi.
30 "Ife tikulonjeza kuti sitidzapereka ana athu aakazi kuti akwatiwe ndi amuna a mayiko ena kapena kutenga ana awo aakazi kuti akwatiwe ndi ana athu aamuna.
31 "Ngati anthu a mitundu ina abwera ndi zinthu za malonda, monga tirigu, kudzagulitsa pa tsiku la Sabata, sitidzawagula pa tsiku la Sabata kapena pa tsiku lina lililonse loyera. Pa chaka chilichonse cha chisanu ndi chiwiri tidzagoneka munda wosawulima ndipo tidzafafaniza ngongole zonse.

32 “Tikulonjezanso molumbira kuti chaka ndi chaka tizipereka magalamu
anayi a siliva kuti zithandize ntchito ya ku Nyumba ya Mulungu wathu.
33 Ndalamayi izithandiza kulipirira buledi wa pa tebulo, chopereka
cha chakudya cha nthawi zonse, zopereka zopsereza za nthawi zonse,
zopereka za pa tsiku la Sabata, za pachikondwerero cha Mwezi
Watsopano, za pa masiku a chikondwerero osankhika, zopereka za
zinthu zopatulika, zopereka za nsembe yopepesera machimo a Aisraeli
ndi ntchito ina iliyonse ya ku Nyumba ya Mulungu.
34 “Ife ansembe, Alevi ndi anthu onse, tachita maere kuti tidziwe pamene
banja lathu lililonse lidzabweretsa ku nyumba ya Mulungu wathu
pa nthawi yoyikika ya chaka zopereka za nkhuni zoyaka pa guwa
lansembe la Yehova Mulungu wathu, monga momwe zinalembedwera
m’Malamulo.”
35 “Tilonjezanso kuti tidzabwera ndi zipatso zoyamba kucha za m’minda
yathu ndi zipatso zoyamba kucha za mtengo uliwonse wa zipatso chaka
ndi chaka kuti tidzapereke ku Nyumba ya Mulungu wathu.”
36 “Tidzabweranso nawo ku Nyumba ya Mulungu, kwa ansembe amene
amatumikira ku Nyumba ya Mulungu ana athu aamuna oyamba
kubadwa ndi ana ang’ombe oyamba kubadwa monga zalembedwera
mu Malamulo. Tidzaperekanso ana oyamba kubadwa a ziweto zathu
ndi ana ankhosa oyamba kubadwa.”
37 “Ndiponso ku zipinda za Nyumba ya Mulungu wathu, kwa ansembe
tidzaperekanso mtanda wathu wa buledi wa ufa ndi mphatso zina
monga zipatso za mtengo uliwonse, vinyo ndi mafuta. Tidzaperekanso
kwa alevi chakhumi cha mbewu zathu pakuti alevi ndiwo amasonkhan-
itsa chakhumi m’midzi yathu yonse. 38 Wansembe, mdzukulu wa Aaroni
azikhala pamodzi ndi Alevi pamene akulandira chakhumi. Ndipo Alevi
azibwera ndi chakhumicho ku nyumba ya Mulungu wathu, kuzipinda
zosungiramo chuma.” 39 Choncho Israeli, kuphatikiza zidzukulu za
Alevi, azipititsa zopereka za tirigu, vinyo ndi mafuta ku zipinda
zosungiramo katundu wopatulika, komanso kokhala ansembe amene
akutumikira pamodzi ndi alonda a ku Nyumba ya Mulungu ndi anthu
oyimba nyimbo.
“Kwambiri ife sitidzaleka kusamala Nyumba ya Mulungu.”

# 11

*Nzika Zatsopano za mu Yerusalemu*

1 Nthawi imeneyo atsogoleri a anthu ankakhala ku Yerusalemu. Tsono
anthu ena onse anachita maere kuti apeze munthu mmodzi pa anthu
khumi aliwonse kuti azikhala ku Yerusalemu, mzinda wopatulika. Anthu
asanu ndi anayi otsalawo ankakhala m’midzi yawo. 2 Anthu anayamikira
onse amene anadzipereka kuti azikhala mu Yerusalemu.
3 Aisraeli wamba, ansembe, Alevi, ogwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu
ndiponso zidzukulu za antchito a Solomoni ankakhala m’midzi yawo,
aliyense mu dera lake. Koma atsogoleri a chigawo cha Yuda anali
atakhazikika mu Yerusalemu. 4 Ku Yerusalemu kunkakhalanso anthu ena
a mafuko a Yuda ndi Benjamini.

Ena mwa zidzukulu za Yuda ndi awa:
Ataya, mwana wa Uziya, mwana wa Zekariya, mwana wa Amariya mwana
wa Sefatiya, mwana wa Mahalaleli. Onsewa anali ana a Perezi. 5 Ena
ndi awa: Maaseya mwana wa Baruki, mwana wa Koli-Hoze mwana wa

Hazaya, mwana wa Adaya, mwana wa Yowaribu, Zekariya mwana wa
Msiloni. [6] Zidzukulu zonse za Perezi, anthu amphamvu zawo amene
ankakhala ku Yerusalemu analipo anthu okwanira 468.

[7] Nazi zidzukulu za Benjamini:
Salu mwana wa Mesulamu, mwana wa Yowedi, mwana wa Pedaya,
mwana wa Kolaya, mwana wa Maaseiya, mwana wa Itieli, mwana wa
Yesaiya. [8] Abale ake anali Gabayi ndi Salaya. Onse pamodzi anali 928.
[9] Yoweli mwana wa Zikiri ndiye anali mtsogoleri wawo, ndipo Yuda
mwana wa Hasenuya ndiye amayang'anira chigawo cha chiwiri cha
mzinda.

[10] Ansembe anali awa:
Yedaya mwana wa Yowaribu; Yakini; [11] Seraya mwana wa Hilikiya mwana
wa Mesulamu, mwana wa Zadoki, mwana wa Merayoti, mwana wa
Ahitubi amene anali woyang'anira Nyumba ya Mulungu, [12] ndi abale
awo, amene ankagwira ntchito ku Nyumba ya Mulungu. Onse pamodzi
anali 822. Panalinso Adaya mwana wa Yerohamu, mwana wa Pelaliya,
mwana wa Amizi, mwana wa Zekariya, mwana wa Pasi-Huri, mwana
wa Malikiya, [13] ndi abale ake, amene anali atsogoleri a mabanja. Onse
pamodzi anali 242. Kuphatikiza apo panalinso Amasisai mwana wa
Azaireli, mwana wa Ahazayi, mwana wa Mesilemoti, mwana wa Imeri
[14] ndi abale ake. Onse pamodzi anali 128 ndipo anali anthu olimba
mtima kwambiri. Mtsogoleri wawo wamkulu anali Zabidieli mwana
wa Hagedolimu.

[15] Alevi anali awa:
Semaya mwana wa Hasubu, mwana wa Azirikamu, mwana wa Hasabiya,
mwana wa Buni. [16] Sabetayi ndi Yozabadi anali atsogoleri amene
ankayang'anira ntchito ya kunja kwa Nyumba ya Mulungu. [17] Mataniya
mwana wa Mika, mwana wa Zabidi, mwana wa Asafu ndiye anali
wotsogolera pa mapemphero achiyamiko. Panalinso Bakibukiya amene
anali wachiwiri pakati pa abale ake. Kuwonjezera apo panalinso Abida
mwana wa Samuwa, mwana wa Galali, mwana wa Yedutuni. [18] Alevi
onse amene anali mu mzinda woyera analipo 284.

[19] Alonda a ku Nyumba ya Mulungu anali awa:
Akubu, Talimoni ndi abale awo. Onse pamodzi anali 172.

[20] Aisraeli ena onse pamodzi ndi ansembe ndi Alevi ankakhala m'mizinda
ya Yuda, ndipo aliyense ankakhala m'dera la makolo ake.

[21] Koma antchito a ku Nyumba ya Mulungu ankakhala pa phiri la Ofeli,
ndipo Ziha ndi Gisipa ndiwo anali kuwayang'anira.

[22] Wamkulu wa Alevi mu Yerusalemu anali Uzi mwana wa Bani, mwana
wa Hasabiya, mwana wa Mataniya, mwana wa Mika. Uzi anali mmodzi
wa zidzukulu za Asafu, amene anali oyimba nyimbo pa nthawi zachipem-
bedzo m'Nyumba ya Mulungu. [23] Pakuti mfumu inalamula kuti tsiku ndi
tsiku pa nthawi zachipembedzo oyimba nyimbowo azikhalapo.

[24] Petahiya mwana wa Mesezabeli, mmodzi mwa zidzukulu za Zera
mwana wa Yuda ndiye ankayimirira Aisraeli pa bwalo la mfumu ya
Perisiya.

25 Anthu ena a fuko la Yuda ankakhala ku Kiriyati-Ariba ndi midzi
yake, ku Diboni ndi midzi yake, ku Yekabizeeli ndi midzi yake, 26 ku
Yesuwa, Molada, Beti-Peleti, 27 Hazari-Suwali, Beeriseba ndi midzi yawo.
28 Ku Zikilagi, Mekona ndi midzi yawo, 29 ku Eni-Rimoni, Zora, Yarimuti,
30 Zanowa, Adulamu ndi midzi yake, ku Lakisi ndi minda yake, ku
Beeriseba mpaka ku chigwa cha Hinomu.
31 Nazonso zidzukulu za Benjamini zinkakhala m'dera lawo kuyambira ku
Geba mpaka ku Mikimasi, Ayiya, Beteli ndi midzi yake, 32 ku Anatoti, Nobu
ndi Ananiya, 33 ku Hazori, Rama ndi Gitaimu, 34 ku Hadidi, Zeboimu ndi
Nebalati, 35 ku Lodi, Ono ndi ku chigwa cha Amisiri.
36 Magulu ena a Alevi a ku Yuda ankakhala ku Benjamini.

# 12

*Ansembe ndi Alevi*

1 Ansembe ndi Alevi amene anabwerera pamodzi ndi Zerubabeli mwana
wa Sealatieli ndi Yesuwa anali awa:
Seraya, Yeremiya, Ezara,
2 Amariya, Maluki, Hatusi,
3 Sekaniya, Rehumu, Meremoti,
4 Ido, Ginetoyi, Abiya
5 Miyamini, Maadiya, Biliga,
6 Semaya, Yowaribu, Yedaya,
7 Salu, Amoki, Hilikiya ndi Yedaya.
Awa ndiye anali atsogoleri a ansembe ndi abale awo pa nthawi ya Yesuwa.
8 Alevi anali Yesuwa, Binuyi, Kadimieli, Serebiya, Yuda, ndiponso
Mataniya, amene pamodzi ndi abale ake ankatsogolera nyimbo za
mayamiko. 9 Abale awo, Bakibukiya ndi Uri, ankayimba nyimbo molan-
dizana.
10 Yesuwa anabereka Yowakimu, Yowakimu anabereka Eliyasibu, Eliya-
sibu anabereka Yoyada. 11 Yoyada anabereka Yonatani, ndipo Yonatani
anabereka Yaduwa.
12 Pa nthawi ya Yowakimu, awa ndiwo anali atsogoleri a mabanja a
ansembe:
Mtsogoleri wa fuko la Seraya anali Meraya;
wa fuko la Yeremiya anali Hananiya;
13 wa fuko la Ezara anali Mesulamu;
wa fuko la Amariya anali Yehohanani;
14 wa fuko la Maluki anali Yonatani;
wa fuko la Sebaniya anali Yosefe;
15 wa fuko la Harimu anali Adina;
wa fuko la Merayoti anali Helikayi;
16 wa fuko la Ido anali Zekariya;
wa fuko la Ginetoni anali Mesulamu;
17 wa fuko la Abiya anali Zikiri;
wa fuko la Miniyamini ndi banja la Maadiya anali Pilitayi;
18 wa fuko la Biliga anali Samuwa;
wa fuko la Semaya anali Yonatani;
19 wa fuko la Yowaribu anali Matenayi;
wa fuko la Yedaya anali Uzi;
20 wa fuko la Salai anali Kalai;

wa fuko la Amoki anali Eberi;
21 wa fuko la Hilikiya anali Hasabiya;
wa fuko la Yedaya anali Netaneli.

22 Pa nthawi ya Eliyasibu, Yoyada, Yohanani ndi Yaduwa panalembedwa
atsogolera a mabanja a Alevi ndi a ansembe mpaka pa nthawi ya ulamuliro
wa Dariyo Mperisi. 23 Zidzukulu za Levi, makamaka atsogoleri a mabanja
awo analembedwa m'buku la mbiri mpaka pa nthawi ya Yohanani mwana
wa Eliyasibu. 24 Ndipo atsogoleri a Alevi awa, Hasabiya, Serebiya, Yesuwa
mwana wa Kadimieli ndi abale awo, ankayimba nyimbo zotamanda
ndi zothokoza molandizana. Gulu limodzi linkavomerezana ndi linzake
monga mmene Davide munthu wa Mulungu analamulira.

25 Mataniya, Bakibukiya, Obadiya, Mesulamu, Talimoni ndi Akubu anali
olonda nyumba zosungiramo chuma pa zipata za ku Nyumba ya Mulungu.
26 Iwo ndiwo ankatumikira pa nthawi ya Yowakimu mwana wa Yesuwa
mwana wa Yozadaki, ndiponso pa nthawi ya bwanamkubwa Nehemiya
ndi wansembe Ezara amene analinso mlembi.

*Mwambo Wopereka Khoma la Yerusalemu*

27 Pa mwambo wopereka khoma la Yerusalemu anayitana Alevi kulikonse
kumene ankakhala kuti abwere ku Yerusalemu ku mwambo wopereka
khoma kwa Mulungu, mwachimwemwe ndi mothokoza poyimba nyimbo
pamodzi ndi ziwiya za malipenga, azeze ndi apangwe. 28 Tsono anthu
a mabanja a Alevi oyimba nyimbo aja anasonkhana pamodzi kuchokera
ku madera onse ozungulira Yerusalemu ndiponso ku midzi ya Anetofati,
29 Beti-Giligala ndi ku madera a ku Geba ndi Azimaveti, pakuti oyimbawo
anali atamanga midzi yawo mozungulira Yerusalemu. 30 Tsono ansembe
ndi Alevi anachita mwambo wodziyeretsa. Pambuyo pake anachita
mwambo woyeretsa anthu onse ndi khoma la Yerusalemu.

31 Ine ndinabwera nawo atsogoleri a dziko la Yuda ndi kukwera nawo
pa khoma. Ndipo ndinasankha magulu awiri akuluakulu oyimba nyimbo
za matamando. Gulu limodzi linadzera mbali ya ku dzanja lamanja
pa khoma mpaka ku Chipata cha Kudzala. 32 Pambuyo pawo panali
Hosayia, theka la atsogoleri a Yuda aja 33 pamodzi ndi Azariya, Ezara,
Mesulamu, 34 Yuda, Benjamini, Semaya ndi Yeremiya. 35 Ena mwa ana a
ansembe amene ankayimba malipenga awo anali awa: Zekariya mwana
wa Yonatani mwana wa Semaya mwana wa Mataniya, mwana wa Mikaya,
mwana wa Zakuri, mwana wa Asafu, 36 pamodzi ndi abale awo awa:
Semaya, Azareli, Milalai, Gilalayi, Maayi, Netaneli, Yuda ndi Hanani. Onse
ankagwiritsa ntchito zida zoyimbira za Davide, munthu wa Mulungu.
Tsono Ezara mlembi uja ankawatsogolera. 37 Kuchokera ku Chipata cha
Kasupe anayenda nakakwera makwerero opita ku mzinda wa Davide pa
njira yotsatira khoma, chakumtundu kwa nyumba ya Davide mpaka ku
Chipata cha Madzi, mbali ya kummawa.

38 Gulu loyimba lachiwiri linadzera mbali ya kumanzere kwa khomalo.
Tsono ine ndi theka lina la atsogoleri aja tinkalitsata pambuyo tikuyenda
pamwamba pa khomalo. Tinapitirira Nsanja ya Ng'anjo mpaka ku Khoma
Lotambasuka. 39 Tinadutsanso Chipata cha Efereimu, Chipata cha Yesana,
Chipata cha Nsomba, Nsanja ya Hananeli, Nsanja ya Zana mpaka kukafika
ku Chipata cha Nkhosa. Ndipo mdipiti uwu unakayima pa Chipata cha
Mlonda.
40 Choncho magulu onse awiri oyimba nyimbo zothokoza aja anakayima
pafupi ndi Nyumba ya Mulungu. Pamodzi ndi ine ndi theka la atsogoleri

aja, 41 panalinso ansembe awa akuyimba malipenga: Eliyakimu, Maaseya,
Miniyamini, Mikaya, Eliyoenai, Zekariya ndi Hananiya. 42 Panalinso
ansembe awa: Maaseya, Semaya, Eliezara, Uzi, Yehohanani, Milikiya,
Elamu ndi Ezeri. Gulu loyimba linkatsogozedwa ndi Yezirahayiya. 43 Pa
tsiku limenelo anthu anapereka nsembe zambiri ndipo anakondwera
chifukwa Mulungu anawapatsa chimwemwe chachikulu. Nawonso akazi
ndi ana anakondwera ndipo kukondwa kwa anthu a mu mzinda wa
Yerusalemu kunamveka kutali.
44 Tsiku limenelo panasankhidwa anthu oyang'anira zipinda zosungiramo
zopereka zaufulu, zipatso zoyamba kucha, zopereka za chakhumi. Anthuwo
ankasonkhanitsa zopereka kuchokera ku minda ya midzi yonse
kuti azipereke kwa ansembe ndi Alevi malingana ndi malamulo. Izi zinali
chomwechi chifukwa Ayuda ankakondwera ndi utumiki wa ansembe
ndi Alevi. 45 Iwowa ankagwira ntchito ya Mulungu wawo, makamaka
mwambo woyeretsa zinthu. Nawonso oyimba nyimbo ndi olonda ku
Nyumba ya Mulungu anagwira ntchito zawo monga Davide ndi mwana
wake Solomoni analamula. 46 Pakuti kalekale, pa nthawi ya Davide
ndi Asafu, panali atsogoleri a anthu oyimba nyimbo za matamando ndi
nyimbo zoyamika Mulungu. 47 Choncho mu nthawi ya Zerubabeli ndi
Nehemiya, Aisraeli onse anakapereka mphatso tsiku ndi tsiku kwa anthu
oyimba nyimbo ndi alonda a ku Nyumba ya Mulungu. Ankayikanso
padera chigawo cha zopereka cha Alevi. Nawonso Alevi ankayika padera
chigawo cha zopereka cha ansembe, zidzukulu za Aaroni.

# 13

*Kukonza Zinthu Kotsiriza kwa Nehemiya*

1 Pa tsiku limenelo anawerenga buku la Mose anthu akumva. Ndipo
anapeza mawu akuti, Mwamoni kapena Mmowabu asalowe konse mu
msonkhano wa Mulungu. 2 Paja iwowa sanawachingamire Aisraeli
kukawapatsa chakudya ndi madzi. M'malo mwake analemba ganyu
Baalamu kuti adzawatemberere. Komabe Mulungu wathu anasandutsa
temberero lo kukhala mdalitso. 3 Anthu atamva lamuloli, anachotsa pakati
pawo onse amene anali achilendo.
4 Izi zisanachitike, wansembe Eliyasibu anali atasankhidwa kukhala
woyang'anira zipinda zosungiramo katundu za Nyumba ya Mulungu.
Iyeyu ankagwirizana kwambiri ndi Tobiya. 5 Choncho anamupatsa
chipinda chachikulu chimene kale ankasungamo zopereka zakudya,
lubani, ziwiya, zopereka za chakhumi za tirigu, vinyo ndi mafuta zoyenera
kuperekedwa kwa Alevi, oyimba nyimbo ndi alonda a ku Nyumba ya
Mulungu, komanso mphatso zoyenera kupereka kwa ansembe.
6 Koma pamene izi zonse zinkachitika mu Yerusalemu, ine kunalibe
popeza m'chaka cha 32 cha Aritasasita mfumu ya Babuloni ine ndinabwerera
kwa mfumu. Patapitanso nthawi ndinapempha chilolezo kwa
mfumuyo 7 ndipo ndinabwerera ku Yerusalemu. Kumeneko ndinamva za
chinthu choyipa chimene Eliyasibu anachita pomupatsa Tobiya chipinda
m'bwalo la Nyumba ya Mulungu. 8 Ndinapsa mtima kwambiri ndipo
ndinataya kunja katundu yense wa Tobiya amene anali m'chipindamo.
9 Ndinalamulira kuti ayeretse zipinda, ndipo kenaka ndinabwezeramo
zida za m'Nyumba ya Mulungu, pamodzi ndi chopereka cha zakudya ndi
lubani.

10 Ndinapezanso kuti Alevi sankalandira magawo awo amene amayera ku-
landira. Chotsatira chake Alevi onse pamodzi ndi oyimba nyimbo amene
ankagwira ku Nyumba ya Mulungu anathawa, aliyense kupita ku munda
wake. 11 Choncho ndinadzudzula akuluakulu aja ndipo ndinawafunsa
kuti, "N'chifukwa chiyani Nyumba ya Mulungu yasiyidwa?" Ndipo ine
ndinawayitanitsa pamodzi ndi kuwayika m'malo awo.
12 Pambuyo pake Ayuda anayambanso kubwera ndi zopereka zawo za
chakhumi cha tirigu, vinyo ndi mafuta kuti ziperekedwe ku nyumba
yosungiramo chuma. 13 Ndipo ndinasankha wansembe Selemiya, mlembi
Zadoki, ndi Mlevi wotchedwa Pedaya kukhala oyang'anira zipinda zo-
sungiramo. Ndinasankhanso Hanani mwana wa Zakuri mwana wa
Mataniya kukhala wowathandizira chifukwa ndinaona kuti anthu awa
anali odalirika. Ntchito yawo inali yogawira abale awo zinthu zofunika.

14 Inu Mulungu wanga, mundikumbukire pa zimenezi, ndipo musafafanize
ntchito zanga zimene ndachita mokhulupirika pa Nyumba yanu pofuna
kukutumikirani.

15 Nthawi imeneyo ndinaona anthu a mu Yuda akuponda ndi kufinya
mphesa pa tsiku la Sabata. Ena ankawunjika tirigu milumilu ndi
kumasenzetsa abulu. Enanso ankabwera ndi vinyo, mphesa, mkuyu ndi
katundu wa mitundumitundu ku Yerusalemu pa tsiku la Sabata. Choncho
ndinawachenjeza za kugulitsa zakudya pa tsiku la Sabata. 16 Nawonso
anthu a ku Turo amene ankakhala mu Yerusalemu ankabweretsa nsomba
ndi akatundu ena onse amalonda kudzagulitsa pa Sabata kwa anthu a
m'dziko la Yuda ndi a mu Yerusalemu. 17 Ndipo ndinadzudzula anthu
olemekezeka a dziko la Yuda. Ndinawafunsa kuti, "N'choyipa chanji
mukuchitachi, kumayipitsa tsiku la Sabata chotere? 18 Makolo anu
anachita zomwezi ndipo Mulungu wathu anadzetsa mavuto pa ife ndi pa
mzinda uwu. Kodi inu mukufuna kuwutsanso mkwiyo wa Mulungu pa
Israeli pamene mukudetsa tsiku la Sabata?"
19 N'chifukwa chake ndikulamula kuti pamene kuyamba kuda, tsiku
la Sabata lisanayambe, azitseka zipata zonse za Yerusalemu ndipo
asazitsekule mpaka sabata litatha. Ndinayika ena mwa antchito anga
oyang'anira pa zipata kuti katundu aliyense asalowe mu Yerusalemu pa
tsiku la Sabata. 20 Choncho kamodzi kapena kawiri anthu amalonda ndi
anthu ogulitsa katundu osiyanasiyana ankagona usiku wonse kunja kwa
Yerusalemu. 21 Koma ndinawachenjeza ndi kuwafunsa kuti, "N'chifukwa
chiyani mukugona pafupi ndi khoma? Ngati muchitanso zimenezi, ine
ndidzakugwirani." Kuyambira nthawi imeneyo, sanabwerenso pa tsiku la
Sabata. 22 Ndipo ndinalamulira Alevi kuti adziyeretse okha ndi kubwera
kudzalonda pa zipata ndi cholinga choti tsiku la Sabata likhale tsiku loyera.

Inu Mulungu wanga, kumbukireninso ine pa zimenezi ndipo mundisunge
malingana ndi chikondi chanu chachikulu chosasinthika.

23 Masiku amenewo ndinaonanso anthu a ku Yuda amene anakwatira
akazi ochokera ku Asidodi, Amoni ndi Mowabu. 24 Theka la ana awo
linkayankhula chiyankhulo cha Asidodi kapena chiyankhulo chimodzi
cha anthu ena, ndipo sankathanso kuyankhula chiyankhulo cha Ayuda.
25 Tsono ndinakangana nawo ndi kuwatemberera. Ndinamenya ena
mwa anthuwo ndi kuzula tsitsi lawo. Ine ndinawalumbiritsa m'dzina

la Mulungu kuti, “Inu musapereke ana anu aakazi kuti akwatiwe ndi
ana awo aamuna kapena inuyo ngakhale ana anu aamuna kukwatira
ana awo aakazi. 26 Kodi Solomoni mfumu ya Israeli suja anachimwa
chifukwa cha ukwati ngati umenewu. Pakati pa mitundu yambiri panalibe
mfumu ngati iyi. Iye anakondedwa ndi Mulungu wake, ndipo Mulungu
anamuyika kukhala mfumu ya Israeli yense, koma iyeyo anachimwa
chifukwa cha akazi achilendo. 27 Kodi tsopano ife tizimva inu kuti
mukuchita choyipa chachikulu chimenechi, kupandukira Yehova Mulungu
wathu pomakwatira akazi achilendo?”
28 Mmodzi mwa ana aamuna a Yehoyada mwana Eliyasibu mkulu wa
ansembe n’kuti nthawi imeneyi ali mpongozi wa Sanibalati wa ku Horoni.
Choncho ndinamuthamangitsa pamaso panga.

29 Inu Mulungu wanga, mukumbukire mmene iwo anayipitsira unsembe,
pangano la unsembe komanso la Alevi.

30 Motero ndinayeretsa ansembe ndi Alevi powachotsera kalikonse
kachilendo. Ndipo ndinakhazikitsa ntchito zawo, kuti aliyense akhale pa
ntchito yake. 31 Ndiponso kupereka nkhuni ndi zipatso zoyamba kucha pa
nthawi yake.

Ndikumbukireni pondikomera mtima, Inu Mulungu wanga.

# Estere

*Vasiti Mkazi wa Mfumu Achotsedwa*

1 Izi ndi zimene zinachitika pa nthawi ya ufumu wa Ahasiwero, amene
analamulira zigawo 127 kuyambira ku India mpaka ku Kusi. 2 Pa nthawi
imeneyi n’kuti mfumu Ahasiwero atakhazikika pa mpando wake wa
ufumu mu mzinda wa Susa, 3 ndipo m’chaka chachitatu cha ufumu wake
anakonza phwando la olemekezeka ndi nduna zake. Atsogoleri a nkhondo
a ku Peresiya ndi Mediya, anthu olemekezeka pamodzi ndi nduna za
m’zigawo zonse anasonkhana kwa iye.

4 Pa nthawi yomweyi kwa masiku 180 a phwando mfumu inkaonetsa
kulemera kwa ulemerero wa ufumu wake ndiponso kukongola ndi kukula
kwa ufumu wake. 5 Atatha masiku amenewa, kwa masiku ena asanu ndi
awiri mfumu inakonzanso phwando la anthu onse okhala mu mzinda wa
Susa kuyambira anthu olemekezeka mpaka anthu wamba ku bwalo la
munda la nyumba yake yaufumu. 6 Bwalo la mundali analikongoletsa ndi
makatani a nsalu zoyera ndi za mtundu wamtambo zimene anaziman-
girira ndi zingwe za nsalu zoyera ndi zapepo ku mphete za siliva zimene
anazikoloweka pa nsanamira za maburo. Anayika mipando yopumirapo
yagolide ndi siliva pabwalo la miyala yoyala yamtengowapatali yofiira,
ya marabulo, ndi yonyezimira. 7 Anapereka zakumwa m’chikho zagolide
zamitundumitundu, ndipo vinyo waufumu anali wochuluka kwambiri
monga mwa kukoma mtima kwa mfumu. 8 Monga mwa lamulo la mfumu
aliyense anamwa m’mene anafunira, pakuti mfumu inawuza otumikira
ake kuti apatse aliyense monga mwa kukonda kwake.

9 Mkazi wa mfumu Vasiti nayenso anakonzera phwando amayi ku
nyumba ya ufumu ya mfumu Ahasiwero.

10 Pa tsiku la chisanu ndi chiwiri, pamene mfumu Ahasiwero inaledzera
ndi vinyo, inalamula adindo ofulidwa asanu ndi awiri amene ankamutu-
mikira: Mehumani, Bizita, Haribona, Bigita, Abagita, Zetara, ndi Karikasi
11 kuti abwere naye mfumukazi Vasiti pamaso pa mfumu atavala chipewa
chaufumu. Cholinga cha mfumu chinali choti adzamuonetse kwa anthu
onse ndi olemekezeka, chifukwa anali wokongola kwambiri. 12 Koma
antchito atapereka uthenga wa mfumu kwa mfumukazi, Vasiti anakana
kubwera. Tsono mfumu inakwiya ndi kupsa mtima.

13 Mfumu inayankhula ndi anthu anzeru ndi ozindikira choyenera
kuchita popeza chinali chikhalidwe chake kufunsa uphungu kwa akatswiri
pa nkhani za malamulo ndi kuweruza kolungama. 14 Anthu amene
ankakhala pafupi ndi mfumu anali awa: Karisena, Setara, Adimata,
Tarisisi, Meresi, Marisena ndi Memukani, olemekezeka asanu ndi awiri
a ku Peresiya ndi Medina amene ankaloledwa mwapadera kuonana ndi
mfumu ndipo anali pamwamba kwambiri mu ufumuwo.

15 Mfumu inafunsa kuti, “Kodi titani naye mfumukazi Vasiti mwa
lamulo, popeza sanamvere lamulo la ine mfumu Ahasiwero limene adindo
ofulidwa anakamuwuza?”

16 Ndipo Memukani anayankha pa maso pa mfumu ndi olemekezeka
anzake kuti, “Mfumukazi Vasiti sanalakwire mfumu yokha, koma walak-
wiranso olemekezeka onse ndi anthu onse okhala m’zigawo zonse za

mfumu Ahasiwero. 17 Pakuti amayi onse adzadziwa zimene wachita
mfumukazi ndipo kotero adzapeputsa amuna awo ndi kunena kuti,
‘Mfumu Ahasiwero analamulira kuti abwere naye mfumukazi Vasiti kwa
iye koma sanapite.’ 18 Lero lomwe lino amayi olemekezeka a ku Peresiya
ndi Mediya amene amva zimene wachita mfumukazi adzaganiza zochita
chimodzimodzi kwa nduna zonse za mfumu. Ndipo kupeputsana ndi
kukongola zidzapitirira.”

19 “Choncho, ngati chikukomerani mfumu, lamulirani kuti Vasiti
asadzaonekerenso pamaso pa mfumu Ahasiwero. Lamuloli lilembedwe
m’mabuku a malamulo a Aperezi ndi Amedi kuti lisadzasinthike. Pamalo
pa Vasiti ngati mfumukazi payikidwepo mkazi wina amene ali bwino
kuposa iye. 20 Ndipo lamulo la mfumuli lilengezedwa m’dziko lake lonse
ngakhale lili lalikulu, amayi onse adzapereka ulemu kwa amuna awo,
amuna olemekezeka mpaka amuna wamba.”

21 Mfumu ndi nduna zake anakondwera ndi uphungu uwu, kotero
mfumu inachita monga momwe ananenera Memukani. 22 Mfumu
inatumiza makalata ku madera onse a ufumu wake, chigawo chilichonse
m’zilembo zawo ndi ku mtundu uliwonse m’chiyankhulo chawochawo ku-
lengeza kuti mwamuna ayankhule chilichonse chimene chikumukomera.

# 2

### *Mfumu Ikwatira Estere*

1 Pambuyo pake mtima wa Ahasiwero utatsika, Ahasiwero anakum-
bukira Vasiti ndi zimene anachita Vasitiyo. Anakumbukiranso lamulo lo-
mukhudza limene anasindikiza. 2 Tsono anyamata a mfumu amene anka-
mutumikira anati, “Mfumu, akufunireni anamwali okongola. 3 Mfumu
isankhe oyang’anira pa chigawo chilichonse cha ufumu wake kuti abwere
nawo pamodzi anamwali onse okongola ku nyumba yosungira akazi ku
Susa. Hegai, mdindo wofulidwa wa mfumu, amene amayang’anira amayi,
akhale wosamalira anamwaliwa ndipo aziwapatsa mafuta odzola. 4 Ndipo
namwali amene mfumu yakondwera naye akhale mfumukazi m’malo
mwa Vasiti.” Mfumu inakondwera ndi uphunguwu, ndipo inachita
momwemo.

5 Myuda wina wa fuko la Benjamini, dzina lake Mordekai, mwana
wa Yairi, mwana wa Simei, mwana wa Kisi, anali mu mzinda wa
Susa. 6 Iyeyu anali mmodzi mwa anthu amene anatengedwa ukapolo
ndi Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni kuchokera ku Yerusalemu
pamodzi ndi Yekoniya mfumu ya Yuda. 7 Mordekai n’kuti atalera
Hadasa, amene ankatchedwanso Estere, mwana wamkazi wa amalume
ake chifukwa analibe abambo kapena amayi. Mtsikanayu anali wokongola
ndi wooneka bwino ndipo Mordekai ankamutenga ngati mwana wake
weniweni pamene abambo ndi amayi ake anamwalira.

8 Lamulo la mfumu atalilengeza ndi kubwera nawo pamodzi anamwali
ambiri ku mzinda wa Susa kuti akasamalidwe ndi Hegai, Estere nayenso
anatengedwa kupita naye ku nyumba ya mfumu kuti akasamalidwe
ndi Hegai woyang’anira nyumba yosungiramo akazi uja. 9 Hegai
anasangalatsidwa naye namwaliyo ndipo anamukomera mtima. Mosa-
taya nthawi anamupatsa mafuta ake odzola ndi chakudya chapadera.
Anamusankhiranso anamwali asanu ndi awiri a ku nyumba ya mfumu

kuti azimutumikira, ndipo iye pamodzi ndi anamwali omutumikira aja anawapatsa malo abwino koposa m'nyumba yosungira akazi.

10 Estere sanawulule mtundu wake ndi abale ake chifukwa Mordekai
anamuletsa kutero. 11 Tsiku ndi tsiku Mordekai ankayendayenda pafupi
ndi bwalo la nyumba yosungiramo akazi ija kuti adziwe za moyo wa Estere ndi kuti zinthu zikumuyendera bwanji.

12 Tsono nthawi inkafika kuti namwali aliyense akaonekere kwa mfumu Ahasiwero, pakutha pa miyezi khumi ndi iwiri yomwe inakhazikitsidwa kuti amayi azidzikongoletsa. Pa miyezi isanu ndi umodzi ankadzola mafuta a mure ndipo pa miyezi isanu ndi umodzi inayo ankadzola
zonunkhira ndi zokongoletsa. 13 Ndipo namwali ankapita kwa mfumu
motere: Ankaloledwa kutenga chilichonse angafune m'nyumba yosungi-
ramo akazi kupita nacho ku nyumba ya mfumu. 14 Ankalowa madzulo
kwa mfumu ndi kutuluka mmawa kupita ku nyumba ina yosungira akazi yomwe ankayang'anira ndi Saasigazi, mdindo wofulidwa wa mfumu amene amayang'anira akazi a mfumu. Namwali sankabwerera kwa mfumu pokhapokha amukomere mtima ndi kumuyitana potchula dzina lake.

15 Tsono inafika nthawi kuti Estere, mwana wamkazi wa Abihaili amenenso analeredwa ndi Mordekai amalume ake, alowe kwa mfumu. Iye sanapemphe kanthu kalikonse, koma anatenga zokhazo zimene ananena Hegai mdindo wofulidwa wa mfumu woyang'anira nyumba yosungiramo
akazi. Ndipo aliyense amene anamuona Estere, anasangalatsidwa naye.
16 Anapita naye kwa mfumu Ahasiwero ku nyumba ya ufumu pa mwezi wa khumi, mwezi wa Tebete, chaka cha chisanu ndi chiwiri cha ufumu wake.

17 Ndipo mfumu inamukonda Estere koposa wina aliyense wa akazi aja, kotero inamukonda ndi kumukomera mtima koposa wina aliyense wa anamwali aja. Choncho anamumveka chipewa chaufumu pa mutu
pake nakhala mfumukazi m'malo mwa Vasiti. 18 Ndipo mfumu inakonza
phwando lalikulu, phwando la Estere, kukonzera anthu olemekezeka ndi nduna zake zonse. Analamuliranso kuti anthu m'zigawo zonse asapereke msonkho ndipo anapereka mphatso monga mwakukoma mtima kwa mfumu.

### *Mordekai Awulula Chiwembu*

19 Anamwali atasonkhanitsidwa pamodzi, Mordekai anakhala pansi pa
chipata cha mfumu. 20 Koma Estere anali asanawululebe za mtundu
wake ndi anthu a pa banja lake monga momwe analamulira Mordekai, chifukwa anapitirira kutsata malangizo a Mordekai monga ankachitira pamene ankamulera.

21 Pa nthawi imene Mordekai ankalondera pa chipata cha mfumu, Bigitana ndi Teresi, awiri mwa adindo ofulidwa amfumu, olondera pa khomo la nyumba yake, anayipidwa mtima ndipo anakonza chiwembu
chofuna kupha mfumu Ahasiwero. 22 Koma Mordekai atazindikira za
chiwembuchi anawuza mfumukazi Estere ndipo iye anakawuza mfumu
m'malo mwa Mordekai. 23 Ndipo pamene anafufuza za chiwembuchi
kuti zinali zoona, adindo awiriwa anaphedwa monyongedwa. Zinthu izi zinalembedwa m'buku la Mbiri ndi kusungidwa ndi Mfumu.

# 3

*Chiwembu cha Hamani Chopha a Yuda*

1 Zitachitika izi, mfumu Ahasiwero anamukweza Hamani mwana wa
Hamedata Mwagagi, anamulemekeza ndikumupatsa mpando wa ulemu
kuposa nduna zina zonse. 2 Atumiki onse a mfumu amene anali pa
chipata cha nyumba ya mfumu ankagwadira ndi kuweramira Hamani
monga mwa lamulo la mfumu. Koma Mordekai sankamugwadira kapena
kumuweramira.

3 Kenaka atumiki a mfumu amene anali pa chipata anafunsa Mordekai
kuti, "Kodi n'chifukwa chiyani sumvera lamulo la mfumu?" 4 Tsiku ndi
tsiku ankayankhula naye koma iye sanamverebe. Choncho anamuwuza
Hamani kuti aone ngati angavomereze khalidwe lotere la Mordekai,
popeza anawawuza kuti anali Myuda.

5 Hamani ataona kuti Mordekai sankamugwadira kapena kumuw-
eramira, anapsa mtima kwambiri. 6 Hamani atamva kuti Mordekai
anali Myuda, anatsimikiza kuti ndi kosakwanira kulanga Mordekai yekha.
M'malo mwake anapeza njira yowonongera Ayuda onse okhala m'dziko
lonse limene mfumu Ahasiwero ankalamulira.

7 Mwezi woyamba, umene ndi mwezi wa Nisani, chaka cha khumi
ndi chiwiri cha ufumu wa Ahasiwero anachita maere, otchedwa Purimu
pamaso pa Hamani kuti apeze tsiku ndi mwezi woyenera. Ndipo maere
anagwera pa mwezi wa khumi ndi chiwiri ndiwo mwezi wa Adara.

8 Kenaka Hamani anakawuza mfumu Ahasiwero kuti, "Pali mtundu
wina wa anthu umene unabalalika ndipo wamwazikana pa mitundu ina
m'zigawo zonse za ufumu wanu umene miyambo yawo ndi yosiyana
ndi ya anthu ena onse ndiponso amene safuna kumvera malamulo a
mfumu, kotero si chinthu cha phindu kuti mfumu iwalekerere anthu otere.
9 Ngati chingakukomereni mfumu, ikani lamulo kuti tiwawononge, ndipo
ndidzalipira matalente 10,000 asiliva mosungiramo chuma cha mfumu za
anthu amene adzachite ntchito imeneyi."

10 Choncho mfumu inavula mphete yodindira ku chala chake ndi
kumupatsa Hamani mwana wa Hamedata Mwagagi, mdani wa Ayuda.
11 Mfumu inati kwa Hamani, "Sunga ndalamazo, ndipo uchite ndi anthuwo
monga ufunira."

12 Alembi analemba zonse zimene Hamani analamula m'makalata
opita kwa akazembe a mfumu, abwanamkubwa a zigawo zonse ndi
kwa oyang'anira mtundu uliwonse wa anthu. Kalatazo zinali za
m'chiyankhulo cha mtundu uliwonse ndipo zinalembedwa m'dzina la
Mfumu Ahasiwero ndi kusindikizidwa ndi mphete yake. 13 Makalatawa
anawatumiza amithenga ku zigawo zonse za mfumu kuti awononge, aphe
ndi kufafaniziratu a Yuda onse, anyamata, anthu okalamba, ana ndi
amayi, pa tsiku limodzi la 13 la mwezi wa Adara ndipo alande katundu
wawo. 14 Mwachidule kalatayi inanena kuti mawu olembedwamowo
anayenera kuperekedwa ngati lamulo m'chigawo chilichonse ndi kuti
anthu a mtundu uliwonse adziwe ndi kukhala okonzeka pa tsikulo.

15 Potsata lamulo la mfumu, amithenga aja anapita mwachangu ndipo
lamuloli linaperekedwanso ku Susa, likulu la dziko. Mfumu ndi Hamani
anakhala pansi ndikumamwa, koma mzinda onse wa Susa unasokonezeka.

# 4

### *Mordekai a Pempha Estere kuti Athandize*

1 Mordekai atamva zonse zimene zinachitika, anang'amba zovala zake,
navala chiguduli ndi kudzola phulusa, ndipo analowa mu mzinda, akulira
mokweza ndi mowawidwa mtima. 2 Ndipo anapita ndi kuyima pa chipata
cha mfumu, chifukwa panalibe wina aliyense amaloledwa kulowa pa
chipata cha mfumu atavala chiguduli. 3 Chigawo chilichonse kumene
mawu a mfumu ndi lamulo lake zinafika, kunali maliro akulu pakati
pa Ayuda. Iwo ankasala zakudya, kulira mofuwula ndi kumadandaula.
Ambiri anavala ziguduli ndi kudzola phulusa.

4 Anamwali otumikira mfumukazi Estere ndi adindo ake ofulidwa
atabwera ndi kumuwuza za Mordekai, anavutika kwambiri. Estere
anamutumizira zovala kuti avale ndi kuti avule chiguduli chake koma
Mordekai sanalole zimenezo. 5 Kenaka Estere anayitana Hataki, mmodzi
wa adindo a mfumu ofulidwa amene anayikidwa kuti azimutumikira
kuti apite kwa Mordekai kuti akamve chimene chimamuvuta komanso
chifukwa chochitira zimenezi.

6 Choncho Hataki anapita kwa Mordekai ku bwalo la mzinda patsogolo
pa chipata cha mfumu. 7 Mordekai anamuwuza zonse zimene zinamu-
chitikira kuphatikizapo mtengo weniweni wa ndalama zimene Hamani
analonjeza kupereka mosungira chuma cha mfumu za anthu amene
adzawononge a Yuda. 8 Mordekai anamupatsanso imodzi mwa makalata
a ulamuliro wonena za chiwembuchi amene anawasindikiza ku Susa
kukamuonetsa ndi kumufotokozera zonse Estere. Anamuwuzanso kuti
akamudandaulire kuti akapite kwa mfumu kukapempha chifundo ndi
kuyidandaulira chifukwa cha anthu a mtundu wake.

9 Hataki anabwerera ndi kumufotokozera Estere zimene Mordekai
ananena. 10 Ndipo Estere anamutuma Hataki kuti akanene kwa Mordekai
kuti, 11 "Atumiki onse amfumu ndi anthu a zigawo za mfumu ankadziwa
kuti mwamuna kapena mkazi aliyense akalowa ku bwalo lake la m'kati
mosayitanidwa ndi mfumu pali lamulo limodzi: lamuloli ndi lakuti
aphedwe. Zimasintha pokhapokha ngati mfumu iloza munthuyo ndi
ndodo yagolide kuti akhale ndi moyo. Koma papita masiku makumi atatu
ndisanayitanidwe ndi mfumu."

12 Tsono Mordekai anawuzidwa mawu a Estere. 13 Kenaka Mordekai
anawawuza kuti akamuyankhe Estere motere: "Usaganize kuti iwe wekha
mwa Ayuda onse udzapulumuka chifukwa chakuti uli m'nyumba ya
mfumu. 14 Pakuti ngati ukhalatu chete nthawi ino, chithandizo ndi
chipulumutso cha Ayuda zidzachokera kwina n'kutheka kuti iwe ndi a
pa banja la makolo ako mudzafa. Ndipo adziwa ndani mwina unalowa
ufumu chifukwa cha nthawi ngati imeneyi?"

15 Pamenepo Estere anatumiza yankho ili kwa Mordekai: 16 "Pitani,
mukasonkhanitse pamodzi Ayuda onse amene ali mu Susa ndipo mundis-
alire chakudya. Musadye kapena kumwa kwa masiku atatu, usiku
ndi usana. Ine ndi anamwali anga onditumikira tidzasala chakudya
monga inu. Izi zikachitika, ine ndidzapita kwa mfumu, ngakhale kutero
ndikutsutsana ndi lamulo. Ndipo ngati n'kufa ndife ndithu."

17 Choncho Mordekai anapita ndi kuchita monga Estere anamupem-
phera.

# 5

*Pempho la Estere kwa Mfumu*

1 Tsiku lachitatu Estere anavala zovala zake zaufumu ndipo anay-
ima m'bwalo la m'kati la nyumba yaufumu choyang'ana ku chipinda
chachikulu cha mfumu. Mfumu inakhala pa mpando waufumu
m'chipinda chachikulu moyang'ana ku chipata cholowera m'nyumba
yaufumu. 2 Mfumu itaona Estere atayima m'bwalomo inakondwera naye
ndipo anamuloza ndi ndodo yagolide imene inali m'dzanja lake. Choncho
Estere anayandikira ndi kukhudza msonga ya ndodoyo.

3 Kenaka mfumu inati kwa iye, "Kodi mukufuna chiyani, inu mfumukazi
Estere? Nanga pempho lanu ndi chiyani? Ngakhale mutapempha theka la
ufumu, ndidzakupatsani."

4 Ndipo Estere anayankha kuti, "Ngati chingakukomereni, mfumu,
mubwere lero pamodzi ndi Hamani kuphwando limene ndakonzera inu
mfumu."

5 Mfumu inati, "Muwuzeni abwere Hamani msanga, kotero kuti tichite
monga Estere wapempha."

Choncho mfumu ndi Hamani anafika kuphwando limene Estere
anakonza. 6 Akumwa vinyo, mfumu inamufunsano Estere kuti, "Kodi
ukupempha chiyani tsopano? Chimene uti upemphe ndikupatsa. Chopem-
pha chako ndi chiti? Ngakhale utafuna mpaka theka la ufumu, ndidzaku-
patsa."

7 Estere anayankha kuti, "Pempho langa ndi chofuna changa ndi ichi:
8 Ngati mwandikomera mtima mfumu ndiponso ngati chingakukondw-
eretseni mfumu kundipatsa chimene ndapempha ndi kuchita zimene
ndifuna, mubwere mawa inu mfumu ndi Hamani ku phwando limene
ndidzakukonzerani. Ndipo ndidzakuyankhani mfumu funso lanu."

*Mkwiyo wa Hamani Ukulabe pa Mordekai*

9 Tsiku limenelo Hamani anatuluka wokondwa ndi wosangalala
kwambiri. Koma ataona Mordekai pa chipata cha mfumu ndi kuti
sanayimirire kapena kumupatsa ulemu pamene iye amadutsa, Hamani
anamukwiyira kwambiri, 10 komabe Hamani anadziletsa ndipo anapita
ku nyumba kwake.

Anayitana abwenzi ake pamodzi ndi mkazi wake Zeresi. 11 Hamani
anawawuza za kuchuluka kwa chuma chake ndi kuti anali ndi ana
aamuna ambiri. Anawawuzanso za mmene mfumu inamukwezera ndi
kumuyika kukhala woposa nduna ndi olemekezeka onse. 12 Hamani
anawonjeza kuti, "Ndipotu si zokhazi. Ndine ndekha amene nday-
itanidwa pamodzi ndi mfumu kuphwando limene mfumukazi Estere
anatikonzera. Ndipo mawa wandiyitananso pamodzi ndi mfumu. 13 Koma
zonsezi sindikhutira nazo ndikamaona nthawi zonse Myuda uja Mordekai
atakhala pa chipata cha mfumu."

14 Mkazi wake Zeresi ndi abwenzi ake onse aja anamuwuza kuti, "Anthu
apange mtanda wotalika mamita 23 ndipo mmawa upemphe mfumu
kuti anthu akhomerepo Mordekai. Kenaka upite ndi mfumu kuphwando
mokondwa." Hamani anakondwera ndi uphungu umenewu ndipo mtanda
unapangidwa.

# 6

*Mordekai Apatsidwa Ulemu*

1 Usiku umenewo mfumu inalephera kugona tulo; Choncho inayitanitsa
buku limene amalembamo mbiri ya zamakedzana kuti amuwerengere.
2 Anapeza kuti m'bukumo munalembedwa zoti Mordekai anawulula kuti
Bigitana ndi Teresi, awiri mwa adindo ofulidwa a mfumu amene ankalon-
dera pa khomo la chipinda cha mfumu ndiwo anakonza chiwembu
chofuna kupha mfumu Ahasiwero.

3 Mfumu inafunsa kuti, "Kodi Mordekai anamupatsa ulemu ndi ukulu
wotani chifukwa cha chinthu chimene anachitachi?"

Atumiki ake anamuyankha kuti, "Palibe chimene chinachitika kwa iye."
4 Mfumu inati, "Kodi ndani ali m'bwalomo?" Tsono Hamani anali
atangolowa kumene m'bwalo lakunja la nyumba yaufumu kuti akawuze
mfumu zomukhomera Mordekai pa mtanda umene anamukonzera.
5 Atumiki ake anamuyankha kuti, "Hamani ndiye wayima mu bwalo."

"Mulowetseni," Mfumu inalamulira.
6 Hamani atalowa, mfumu inamufunsa kuti, "Kodi timuchitire ulemu
otani munthu amene mfumu ikondweretsedwa naye?"

Tsono Hamani anaganiza mu mtima kuti, "Kodi palinso ndani amene
mfumu ingamulemekeze kuposa ine?" 7 Choncho Hamani anayankha mfu-
muyo kuti, "Munthu amene mfumu ifuna kumuchitira ulemu, imuchitire
izi: 8 Anthu abwere ndi chovala cha ufumu ndi kavalo amene mfumu
imakwerapo wokhala ndi chizindikiro chaufumu pamutu pake. 9 Ndipo
mupereke chovala cha ufumucho ndi kavalo kwa mmodzi wa akalonga a
mfumu a ulemu kwambiri. Ameneyu amuveke chovalacho munthu amene
mfumu yakondweretsedwa naye. Akavekedwa chovalachi amuyendetse
m'misewu yonse ya mzinda atakwera pa kavalo wa mfumu. Kalongayu
azifuwula patsogolo pa munthuyu kuti 'Ichi ndi chimene mfumu yachita
kwa munthu amene yafuna kumuchitira ulemu!' "

10 Mfumu inalamulira Hamani kuti, "Pita msanga, katenge chovala cha
ufumu ndi kavalo ndipo uchite monga wanenera kwa Mordekai Myuda,
amene amakhala pa chipata cha mfumu. Usasiyeko china chilichonse
chimene wanena."

11 Choncho Hamani anatenga chovala ndi kavalo. Anamuveka Mordekai
chovalacho ndipo anamuyendetsa m'misewu yonse ya mu mzinda atak-
wera pa kavalo, akufuwula kuti, "Ichi ndi chimene mfumu yachita kwa
munthu amene yafuna kumuchitira ulemu!"

12 Pambuyo pake Mordekai anabwerera ku chipata cha mfumu. Koma
Hamani anapita msanga ku nyumba kwake, akulira, atafundira mutu
wake. 13 Hamani anawuza Zeresi mkazi wake ndi abwenzi ake onse zonse
zinamuchitikira.

Anthu ake anzeru ndi mkazi wake Zeresi anamuwuza kuti, "Popeza kuti
Mordekai ndi Myuda amene mwayamba kale kugonja pamaso pake, ndiye
kuti palibe chimene mungachitepo. Mudzagwa ndithu pamaso pake."
14 Pamene anthuwa amayankhula nayebe, adindo a mfumu ofulidwa
anabwera kudzamutenga Hamani mofulumira kupita naye ku phwando
limene Estere anakonza.

# 7

*Hamani Aphedwa*

1 Choncho mfumu ndi Hamani anabwera kudzadya phwando la mfu-
mukazi Estere. 2 Pa tsiku lachiwiri akumwa vinyo, mfumu inafun-
sanso kuti, “Kodi iwe mfumukazi Estere, chimene ufuna kupempha
n’chiyani? Chimene uti upemphe ndidzakupatsa. Choncho ukufuna
chiyani? Ngakhale utafuna theka la ufumu ndidzakupatsa.”
3 Kenaka mfumukazi Estere anayankha kuti, “Ngati mwandikomera
mtima, inu mfumu, ndipo ngati chingakukomereni mfumu, pempho ndi
chokhumba changa ndi ichi, mulole kuti ine ndi abale anga tisungidwe
tonse ndi moyo. 4 Popeza ine ndi anthu a mtundu wanga tagulitsidwa
kuti atiwononge, atiphe ndi kutifafaniziratu. Akanangotigulitsa kokha
tikanakhala chete, chifukwa chimene mdani wathuyo akanakupatsani
mfumu sibwenzi mutasowa nacho mtendere.”
5 Mfumu Ahasiwero anamufunsa mfumukazi Estere, “Kodi iyeyu ndi
ndani ndipo ali kuti amene saopa kuchita chinthu chotere?”
6 Estere anati, “Wotizunza ndiponso mdani wathu! Munthu woyipayo
ndi Hamani.”
Kenaka Hamani anagwidwa ndi mantha pamaso pa mfumu ndi mfu-
mukazi. 7 Mfumu itakwiya kwambiri inanyamuka pa phwando nipita ku
munda wa maluwa wa nyumba yaufumu. Koma Hamani, pozindikira
kuti mfumu yaganiza kale kumuchitira choyipa, anatsalira m’nyumba
kupempha Estere kuti apulumutse moyo wake.
8 Mfumu itabwerera kuchokera ku munda wa maluwa wa nyumba
yaufumu uja ndi kulowanso m’chipinda chaphwando, anapeza Hamani
atagona chafufumimba pa mpando wa khutagone pomwe Estere anakha-
lapo.
Mfumu inayankhula mokweza kuti, “Kodi afunanso kuvula mfumukazi
momukakamiza pamene ine ndili m’nyumba?”
Mfumu isanatsirize kuyankhula mawu awa, atumiki ake anaphimba
nkhope ya Hamani. 9 Haribona, mmodzi wa adindo ofulidwa amene
ankatumikira mfumu anati, “Mtanda wotalika mamita 23 uli m’nyumba
ya Hamani. Mtandawu, Hamani anapangira Mordekai, uja amene
anapulumutsa mfumu ku chiwembu.”
Mfumu inati, “Mpachikeni pamenepo!” 10 Choncho anamupachika
Hamani pa mtanda umene anakonzera Mordekai. Kenaka mkwiyo wa
mfumu unatsika.

# 8

*Lamulo la Mfumu Lothandiza Ayuda*

1 Tsiku lomwelo mfumu Ahasiwero anamupatsa mfumukazi Estere
nyumba ya Hamani, mdani wa Ayuda. Ndipo Mordekai anafika pamaso pa
mfumu, popeza Estere anamuwuza ubale wawo. 2 Mfumu inavula mphete
yake yodindira imene analanda kwa Hamani ndipo Estere anamusankha
Mordekai kukhala woyang’anira nyumba ya Hamani.
3 Estere anayankhulanso ndi mfumu ndipo anadzigwetsa pa mapazi
ake. Uku akulira iye anapempha mfumu kuti iletse choyipa, makamaka
chiwembu chimene Hamani Mwagagi anakonza kuti awononge a Yuda.
4 Ndipo mfumu inamuloza Estere ndi ndodo yake yagolide ndipo Estere
anadzuka ndi kuyima pamaso pake.
5 Iye anati, “Ngati chikomera mfumu ndi kukukondweretsani, ngati
pempho langa muliona kuti ndi loyenera ndi kuti mukondwera nane tsono

mfumu ilole kuti lamulo lilembedwe kusintha mawu a m'makalata amene
Hamani mwana wa Hamedata, Mwagagi, anatumiza ku zigawo zonse za
mfumu. Paja Hamani analemba kuti Ayuda onse awonongedwe. [6] Kodi
ndingapirire bwanji pamene ndi kuona tsoka likugwera anthu a mtundu
wanga? Ndingapirire bwanji pamene abale anga akuwonongedwa?"

[7] Mfumu Ahasiwero anamuyankha mfumukazi Estere ndi Mordekai
Myuda kuti, "Ndapereka nyumba ya Hamani kwa Estere ndipo Hamaniyo
amupachika kale pa mtanda chifukwa anafuna kuwononga Ayuda.
[8] Tsono inu awiri, lembani za Ayudawo monga mufunira. Mulembe
m'dzina la mfumu ndipo musindikize chizindikiro cha mphete ya mfumu
popeza kuti cholembedwa m'dzina la mfumu ndi kusindikizidwa ndi
chizindikiro cha mphete ya mfumu sichingasinthidwe."

[9] Nthawi yomweyo, pa tsiku la 23 la mwezi wachitatu wa Sivani, mfumu
inayitana alembi ake. Analemba zonse zokhudza Ayuda monga ananenera
Mordekai. Analembera akazembe, abwanamkubwa ndi nduna za zigawo
127 kuyambira ku India mpaka ku Kusi. Zimene analamula Mordekai
zinalembedwa m'zilembo za chigawo chilichonse ndi chiyankhulo cha
mtundu uliwonse wa anthu. Ayudanso anawalembera m'malemba awo
ndi chiyankhulo chawo. [10] Mordekai analemba makalatawo m'dzina la
mfumu Ahasiwero, nawadinda ndi chizindikiro cha mphete ya mfumu.
Ndipo anawatumiza ndi anthu amithenga amene anakwera pa akavalo a
ufumu othamanga kwambiri obadwa mu khola la ufumu.

[11] M'makalata amenewa mfumu inalola kuti Ayuda okhala mu mzinda
uliwonse akhale ndi ufulu wokumana ndi kudzitchinjiriza komanso
kuwononga, kupha ndi kufafaniziratu gulu lililonse la nkhondo la anthu
a mtundu uliwonse kapena chigawo chimene chingawathire nkhondo.
Ayudawo analoledwa kuwononga gulu lankhondo lija, ana awo ndi akazi
awo komanso kuti afunkhe katundu wawo. [12] Ayuda analoledwa kuchita
zimenezi m'zigawo zonse za Mfumu Ahasiwero pa tsiku limodzi lokha la
13 la mwezi wa 12, mwezi wa Adara. [13] Mawu a m'makalatawo anayenera
kudziwitsidwa kwa anthu a mtundu uliwonse mu chigawo chilichonse kuti
ndi lamulo ndithu kwa anthu a mtundu uliwonse ndi kuti Ayuda adzakhale
okonzeka pa tsikulo kulipsira kwa adani awo.

[14] Atawalamulira a mfumu, amithenga aja anapita nawo makalata
mwachangu, atakwera pa akavalo a mfumu. Ndipo lamulolo
analiperekanso ku likulu la mzinda wa Susa.

[15] Mordekai anachoka pamaso pa mfumu atavala zovala zaufumu
zooneka ngati mtambo ndi zofewa zoyera, chipewa chachikulu cha golide
ndi mkanjo wapepo. Ndipo mzinda wa Susa unafuwula mokondwa.
[16] Kwa Ayuda inali nthawi ya nkhope zowala ndi za chimwemwe,
chikondwerero ndi ulemu. [17] M'chigawo chilichonse ndi mu mzinda
uliwonse, kumene mawu a mfumu onena za lamulo lake anafika, kunali
chimwemwe ndi chikondwerero pakati pa Ayuda. Linali tsiku la phwando
ndi chikondwerero. Ndipo anthu ambiri a mitundu ina anazitcha Ayuda
chifukwa anachita mantha ndi Ayudawo.

# 9

*Chigonjetso cha Ayuda*

[1] Pa mwezi wa 12, mwezi wa Adara pa tsiku la 13 la mwezi womwewo,
tsiku limene lamulo loyamba lija la mfumu linayembekezereka kuti

litsatidwe, pamene adani a Ayuda anati awononge Ayudawo, zinthu
zinasintha. Ayuda ndiwo anawononga adani awo. 2 Ayuda anasonkhana
m'mizinda ya zigawo zonse za Mfumu Ahasiwero kuthira nkhondo
onse amene anafuna kuwawononga. Palibe amene akanalimbana nawo
chifukwa anthu onse a mitundu ina anachita nawo mantha. 3 Ndipo
akuluakulu onse a zigawo, akalonga, akazembe ndi ogwira ntchito za
mfumu anathandiza Ayuda, chifukwa anachita mantha ndi Mordekai.
4 Pajatu Mordekai anali munthu wamkulu m'nyumba ya ufumu. Mbiri
yake inafalikira zigawo zonse, ndipo mphamvu zake zinakulirakulirabe.

5 Motero Ayuda anakantha adani awo onse ndi lupanga, kuwapha ndi
kuwawononga, ndipo anachita chimene chinawakomera kwa adani awo.
6 Ku likulu la mzinda wa Susa, Ayuda anapha ndi kuwononga anthu
500. 7 Ayuda anaphanso Parisandata, Dalifoni, Asipata, 8 Porata, Adaliya,
Aridata, 9 Parimasita, Arisai, Aridai ndi Vaisata, 10 ana khumi a Hamani,
mwana wa Hamedata, mdani wa Ayuda. Koma sanalande katundu wawo.

11 Tsiku lomwelo anawuza mfumu chiwerengero cha anthu amene
anaphedwa mu likulu la mzinda wa Susa. 12 Mfumu inati kwa mfumukazi
Estere, "Ayuda apha ndi kuwononga anthu 500 ndi ana khumi a Hamani
mu likulu la mzinda wa Susa. Nanga ku zigawo zina zonse za mfumu
achitako chiyani? Kodi tsopano ukupemphanso chiyani? Chimene
ukupempha ndidzakupatsa. Kodi ukufuna chiyani? Chimene ukufuna
ndidzakupatsa."

13 Estere anayankha kuti, "Ngati chingakukomereni mfumu, apatseni
chilolezo Ayuda okhala mu Susa kuti achitenso zimene achita lerozi mawa,
potsata lamulo ndipo mulole kuti ana khumi a Hamani aja mitembo yawo
ipachikidwe pa mtanda."

14 Choncho mfumu inalamula kuti izi zichitike. Anapereka lamulo mu
Susa ndipo mitembo ya ana khumi a Hamani anayipachika pa mtanda.
15 Ayuda a mu mzinda wa Susa anasonkhana pamodzi pa tsiku la 14
la mwezi wa Adara ndipo anapha anthu 300 mu Susa, koma sanatenge
katundu wawo.

16 Tsono Ayuda ena onse amene anali mu zigawo za mfumu ana-
sonkhananso kudziteteza ndipo sanasautsidwenso ndi adani popeza
anapha anthu 75,000 koma sanalande zofunkha zawo. 17 Zonsezi zina-
chitika pa tsiku la 13 la mwezi wa Adara ndipo pa tsiku la 14 anapumula
ndi kupanga tsikuli kuti likhale la madyerero ndi chikondwerero.

### *Kukondwerera Purimu*

18 Koma Ayuda okhala mu Susa anasonkhana pa tsiku la 13 ndi la
14 ndipo anakonza tsiku la 15 kuti likhale tsiku la madyerero ndi
chikondwerero.

19 Ichi ndi chifukwa chake Ayuda a ku midzi, amene amakhala
m'zithando amasunga tsiku la 14 la mwezi wa Adara ngati la madyerero
ndi chikondwerero, tsiku lopatsana mphatso.

20 Mordekai analemba mawu awa m'makalata ndipo anawatumiza kwa
Ayuda onse okhala m'zigawo zonse za mfumu Ahasiwero, a pafupi ndi
a kutali: 21 Anati chaka chilichonse, Ayudawo azisunga tsiku la 14 ndi
15 la mwezi wa Adara, 22 ngati masiku amene Ayuda anapulumutsidwa
kwa adani awo, ndiponso ngati mwezi umene chisoni chawo chinasan-
dulika chimwemwe ndi kulira kwawo kunasandulika chikondwerero.
Anawalembera kuti azisunga masikuwa ngati masiku a madyerero ndi

chikondwerero, masiku opatsana mphatso zachakudya kwa wina ndi
mnzake komanso opereka mphatso kwa osauka.
[23] Choncho Ayuda anavomereza kusunga masikuwa ngati a chikondw-
erero monga analembera Mordekai. [24] Hamani mwana wa Hamedata,
Mwagagi, mdani wa Ayuda onse, anakonza chiwembu chakupha ndi
kuwononga Ayuda ndipo anachita maere otchedwa Purimu kuti awaphe
ndi kuwawononga. [25] Koma mfumu itazindikira za chiwembuchi,
inalamula kuti zilembedwe m'makalata kuti chiwembu chimene Hamani
anakonzera Ayuda chigwere pa iye mwini, ndi kuti iye pamodzi ndi ana
ake apachikidwe pa mtanda. [26] Ndi chifukwa chake masiku amenewa
amatchedwa masiku a Purimu potsata dzina lakuti Purimu. Chifukwa
cha kalata ya Mordekai ndiponso chifukwa cha zimene anaziona ndi
kuwachitikira, [27] Ayuda onse anagwirizana kukhazikitsa lamulo lokhudza
iwo, zidzukulu zawo ndi onse amene adzapanga nawo ubale kuti
asalephere kusunga masiku awiri amenewa chaka chilichonse monga
zinalembedweramo ndiponso potsata nthawi imene anayika. [28] Azisunga
ndi kukumbukira masiku amenewa mu m'bado uliwonse ndi banja
lililonse, m'chigawo chilichonse ndi mu mzinda uliwonse. Ndipo Ayuda
asadzasiye kukondwerera masiku a Purimuwa ndiponso zidzukulu zawo
zisadzaleke kuwakumbukira.
[29] Choncho mfumukazi Estere, mwana wa mkazi wa Abihaili, pamodzi
ndi Mordekai Myuda analemba ndi ulamuliro onse kutsimikizira kalata
iyi yachiwiri yokhudza Purimu. [30] Ndipo Mordekai anatumiza makalata
kwa Ayuda onse ku zigawo 127 za ufumu wa Ahasiwero. Kalatayi inali
ya mawu a mtendere ndiponso a kukhulupirika [31] kuti azisunga masiku a
Purimu pa nyengo imene inavomerezeka monga mmene Mordekai Myuda
ndi mfumukazi Estere anawalamulira ndiponso monga anadziyikira eni
okha ndi zidzukulu zawo zonena za nthawi zawo za kusala zakudya ndi
kulira. [32] Lamulo la Estere linakhazikitsa mwambo wa Purimuwu ndipo
zinalembedwa m'mabuku.

# 10

*Ukulu wa Mordekai*

[1] Mfumu Ahasiwero anakhometsa msonkho m'dziko lake lonse mpaka
ku zilumba zonse. [2] Ndipo ntchito zonse zochitika ndi mphamvu zake
komanso ndi zonse zofotokoza za ukulu wa Mordekai, kukwezedwa kwake
ndi mfumu, kodi sizinalembedwe m'buku la mbiri ya mafumu a ku Mediya
ndi Peresiya? [3] Pakuti Mordekai Myuda uja anali wachiwiri wa mfumu
Ahasiwero. Kwa Ayuda onse Mordekai anali munthu wamkulu ndipo
ankamukonda chifukwa ankachitira zabwino mtundu wake ndi kufunira
mtendere abale ake.

# Yobu

*Mawu Oyamba*

1 M'dziko la Uzi munali munthu wina, dzina lake Yobu. Munthu
ameneyu anali wosalakwa ndi wolungama mtima, ankaopa Mulungu ndi
kupewa zoyipa. 2 Anali ndi ana aamuna asanu ndi awiri ndi ana aakazi
atatu, 3 ndipo anali ndi nkhosa 7,000, ngamira 3,000, ng'ombe zantchito
1,000 ndi abulu aakazi 500, ndiponso anali ndi antchito ambiri. Iye
anali munthu wotchuka kwambiri pakati pa anthu onse a m'mayiko a
kummawa.
4 Ana ake aamuna ankachita phwando mosinthanasinthana m'nyumba
zawo, ndipo ankayitana alongo awo atatu aja kudzadya ndi kumwa
nawo. 5 Masiku aphwandowo atatha, Yobu ankawayitana kuti adzaway-
eretse. Mmamawa iye ankapereka nsembe yopsereza kuperekera mwana
aliyense, poganiza kuti, "Mwina ana anga achimwa ndi kutukwana
Mulungu m'mitima yawo." Umu ndi mmene Yobu ankachitira nthawi
zonse.

*Yobu Ayesedwa Koyamba*

6 Ana a Mulungu atabwera kudzadzionetsa pamaso pa Yehova, nayenso
Satana anafika nawo limodzi. 7 Yehova anati kwa Satanayo, "Kodi iwe
ukuchokera kuti?"
Satana anayankha Yehova kuti, "Ndakhala ndikungoyendayenda ndi
kumangozungulira m'dzikoli."
8 Pamenepo Yehova anati kwa Satana, "Kodi unalingalirapo za mtumiki
wanga Yobu? Palibe wina pa dziko lapansi wofanana naye; ndi munthu
wosalakwa ndi wolungama mtima, munthu amene amaopa Mulungu ndi
kupewa zoyipa."
9 Satana anayankha kuti, "Kodi Yobu amaopa Mulungu popanda
chifukwa?" 10 "Kodi Inu simumamuteteza iyeyo, nyumba yake ndi zonse
zimene ali nazo? Mwadalitsa ntchito ya manja ake, kotero kuti nkhosa ndi
ng'ombe zake zili ponseponse m'dzikomo. 11 Koma tatambasulani dzanja
lanu ndi kukantha zonse ali nazo ndipo iyeyo adzakutukwanani ndithu
pamaso panu."
12 Yehova anati kwa Satana, "Chabwino, tsono zonse zimene ali nazo
ndaziyika m'manja mwako, koma iye yekhayo usamukhudze."
Pamenepo Satana anachoka pamaso pa Yehova.
13 Tsiku lina pamene ana aamuna ndi ana aakazi a Yobu ankachita
phwando ndi kumwa vinyo m'nyumba mwa mkulu wawo, 14 wamthenga
anabwera kwa Yobu ndipo anati, "Ng'ombe zanu zotipula ndipo abulu
anu amadya chapafupi pomwepo, 15 tsono panabwera Aseba kudzatithira
nkhondo ndi kutenga zonse. Apha antchito ndi lupanga, ndipo ine ndekha
ndiye ndapulumuka kuti ndidzakuwuzeni!"
16 Iyeyo akuyankhulabe, wamthenga wina anabwera nati, "Kunagwa
mphenzi ndipo yapsereza nkhosa ndi antchito anu onse, ndipo ine ndekha
ndiye ndapulumuka kuti ndidzakuwuzeni!"
17 Iyeyo akuyankhulabe, wamthenga wina anabwera nati, "Akasidi
anadzigawa m'magulu atatu ankhondo ndipo anafika pa ngamira zanu
ndi kuzitenga. Apha antchito anu onse ndi lupanga, ndipo ine ndekha
ndiye ndapulumuka kuti ndidzakuwuzeni!"

18 Iyeyo akuyankhulabe, panafikanso wamthenga wina nati, “Ana anu
aamuna ndi aakazi amachita phwando ndi kumwa vinyo m’nyumba
ya mkulu wawo, 19 mwadzidzidzi chinayamba chimphepo champhamvu
chochokera ku chipululu, n’kudzawomba nyumba mbali zonse zinayi.
Nyumbayo yawagwera ndipo afa, ndipo ine ndekha ndiye ndapulumuka
kuti ndidzakuwuzeni!”
20 Atamva zimenezi, Yobu anayimirira nang’amba mkanjo wake, ndi
kumeta tsitsi lake. Kenaka anadzigwetsa pansi napembedza Mulungu,
21 nati,

“Ndinatuluka maliseche m’mimba mwa amayi anga,
namonso m’manda ndidzalowa wamaliseche.
Yehova ndiye anapereka ndipo Yehova watenga;
litamandike dzina la Yehova.”

22 Mu zonsezi, Yobu sanachimwe kapena kunena kuti, “Mulungu
walakwa.”

# 2

## *Yobu Ayesedwa Kachiwiri*

1 Tsiku linanso pamene ana a Mulungu anabwera kudzadzionetsa pa-
maso pa Yehova, nayenso Satana anabwera nawo limodzi kudzadzionetsa
pamaso pa Yehova. 2 Ndipo Yehova anati kwa Satana, “Kodi iwe
ukuchokera kuti?”

Satana anayankha Yehova kuti, “Ndakhala ndikungoyendayenda ndi kumangozungulira m’dzikoli.”

3 Pamenepo Yehova anati kwa Satana, “Kodi unalingalirapo za mtumiki
wanga Yobu? Palibe wina pa dziko lapansi wofanana naye; ndi munthu
wosalakwa ndi wolungama mtima, munthu amene amaopa Mulungu
ndi kupewa zoyipa. Ndipo iye akanalibe wangwiro, ngakhale iwe
unandiwumiriza kuti ndikulole kuti umuvutitse popanda chifukwa.”
4 Satana anayankha kuti, “Iye ayesedwe m’thupi mwake. Munthu
angathe kupereka zonse ali nazo malingana iyeyo ali ndi moyo. 5 Koma
tatambasulani dzanja lanu ndi kuwononga thupi lake, ndipo iyeyo
adzakutukwanani ndithu pamaso panu.”
6 Yehova anati kwa Satana, “Chabwino, iye ali m’manja mwako; koma
moyo wake usawuchotse.”
7 Choncho Satana anachoka pamaso pa Yehova napita kukazunza Yobu
ndi zilonda zaululu pa thupi lake lonse. 8 Pamenepo Yobu anatenga phale
ndi kumadzikanda nalo atakhala pa dzala la phulusa.
9 Mkazi wake anati kwa iye, “Kodi ukuwumirirabe kukhala wangwiro?
Tukwana Mulungu kuti ufe!”
10 Yobu anayankha kuti, “Ukuyankhula ngati mkazi wopusa. Kodi
tidzalandira zokoma zokhazokha kwa Mulungu, osalandiranso zowawa?”

Mu zonsezi, Yobu sanachimwe pa zimene anayankhula.

## *Abwenzi Atatu a Yobu*

11 Abwenzi atatu a Yobu, Elifazi wa ku Temani, Bilidadi wa ku Suki
ndi Zofari wa ku Naama, atamva za tsoka lonse limene linamugwera iye,
ananyamuka ku nyumba zawo nakumana malo amodzi mopangana kuti
apite ndi kukamupepesa Yobu ndi kumutonthoza. 12 Atamuona Yobuyo,
iwo ali chapatalipo, sanathe kumuzindikira. Choncho anayamba kulira
mokweza mawu ndipo anang’amba mikanjo yawo ndi kuwaza fumbi pa
mitu yawo. 13 Tsono anakhala naye pamodzi pansi kwa masiku asanu ndi

awiri, usana ndi usiku omwe. Palibe ndi mmodzi yemwe anayankhula naye, chifukwa anazindikira kuti Yobu amavutika kwambiri.

# 3

*Mawu a Yobu*

1 Pambuyo pake Yobu anatsekula pakamwa pake nayamba kutemberera
tsiku limene iyeyo anabadwa. 2 Ndipo Yobu anati:

3 "Tsiku limene ine ndinabadwa litembereredwe
ndi usiku umene ananena kuti, 'Mwana wamwamuna wabadwa!'
4 Tsiku limenelo lisanduke mdima;
Mulungu wa kumwambako asalilabadirenso;
kuwala kusaonekenso pa tsikulo.
5 Mdima ndi mthunzi wa imfa zikhale pa tsiku limeneli;
mtambo uphimbe tsikuli;
mdima wandiweyani udetse kuwala kwake.
6 Usiku umenewo ukutidwe ndi mdima wandiweyani;
usawerengedwenso pamodzi ndi masiku a chaka,
kapena kukhala pa mwezi wina uliwonse.
7 Usiku umenewo usabweretse chilichonse chabwino;
kusamvekenso nthungululu za chikondwerero.
8 Odziwa kutemberera masiku alitemberere tsikulo,
iwo amene akonzekera kuwutsa Leviyatani.
9 Nyenyezi zake za m'bandakucha zikhale mdima;
tsikulo liyembekezere kucha pachabe
ndipo lisaonenso kuwala koyamba kwa m'bandakucha.
10 Pakuti tsiku limenelo ndiye ndinatuluka m'mimba ya amayi anga
ndipo ndi limene linandionetsa zovuta.

11 "Bwanji ine sindinawonongeke pamene ndinkabadwa
ndi kufa pamene ndimatuluka m'mimba?
12 Chifukwa chiyani panali mawondo wondilandirirapo
ndi mawere woti andiyamwitsepo?
13 Pakuti tsopano bwenzi ndili gone mwamtendere;
ndikanakhala nditagona tulo ndili pa mpumulo
14 pamodzi ndi mafumu ndi aphungu a dziko lapansi,
amene anadzimangira nyumba zikuluzikulu zimene tsopano ndi mabwinja,
15 pamodzi ndi olamulira amene anali ndi golide,
amene anadzaza nyumba zawo ndi siliva.
16 Kapena, bwanji sindinakwiriridwe pansi monga mwana wobadwa wakufa kale,
ngati khanda limene silinaone kuwala kwa dzuwa?
17 Ku mandako anthu oyipa sakhalanso pa mavuto,
ndipo kumeneko anthu otopa ali pa mpumulo.
18 A m'ndende kumeneko akusangalala ndi mtendere;
sakumvanso mawu ofuwula a kapitawo wa akapolo.
19 Anthu wamba ndi anthu apamwamba ali kumeneko,
ndipo kapolo ndi womasuka kwa mbuye wake.

20 "Chifukwa chiyani dzuwa limawalira iwo amene ali pa mavuto,
ndipo moyo umapatsidwa kwa owawidwa mtima,

21 kwa iwo amene amalakalaka imfa imene sibwera,
amene amayifunafuna imfayo kupambana chuma chobisika,
22 amene amakondwa ndi kusangalala
akamalowa m'manda?
23 Chifuwa chiyani moyo umaperekedwa kwa munthu
amene njira yake yabisika,
amene Mulungu wamuzinga ponseponse?
24 M'malo moti ndidye, ndimalira,
ndi kubuwula kwanga n'kosalekeza.
25 Chimene ndinkachiopa chandigwera;
chimene ndinkachita nacho mantha chandichitikira.
26 Ndilibe mtendere kapena bata,
ndilibe mpumulo, koma mavuto okhaokha."

# 4

*Mawu a Elifazi*

1 Pamenepo Elifazi wa ku Temani anayankha kuti,
2 "Ngati wina atakuyankha, kodi ungakhumudwe?
Koma ndani angakhale chete wosayankhula?
3 Taganiza momwe iwe walangizira anthu ambiri,
momwe walimbitsira anthu ofowoka.
4 Mawu ako analimbitsa anthu ofuna kugwa;
unachirikiza anthu wotha mphamvu.
5 Koma tsopano mavuto akufikira ndipo wataya mtima,
zakukhudza ndipo uli ndi mantha.
6 Kodi kuopa Mulungu kwako sindiko kulimbika mtima kwako?
Ndipo moyo wako wosalakwa ndiye chiyembekezo chako?

7 "Ganiza bwino tsopano: Kodi munthu wosalakwa anawonongekapo n'kale lonse?
N'kuti kumene munthu wolungama mtima anaphedwa?
8 Monga ndaonera ine, anthu amene amatipula zoyipa,
ndi iwo amene amadzala mavuto, amakolola zomwezo.
9 Iwo amaphedwa ndi mpweya wa Mulungu;
amawonongeka ndi mpweya waukali wa mkwiyo wake.
10 Mikango imabangula ndi kulira,
komabe mano a mikango yamphamvu amathyoledwa.
11 Mkango umafa chifukwa chosowa nyama,
ndipo ana amkango amamwazikana.

12 "Mawu anabwera kwa ine mwamseri,
makutu anga anamva kunong'ona kwake.
13 M'kati mwa maloto ochititsa mantha usiku,
nthawi imene anthu amagona tulo tofa nato,
14 ndinagwidwa ndi mantha, ndi kuyamba kunjenjemera
ndipo mafupa anga onse anaweyeseka.
15 Pamenepo mzimu unadutsa pamaso panga,
ndipo ubweya wa pa thupi langa unayima kuti njoo.
16 Chinthucho chinayimirira
koma sindinathe kuzindikira kuti chinali chiyani.
Chinthu chinayima patsogolo panga,

kunali zii ndipo ndinamva mawu akuti,
17 ‘Kodi munthu angathe kukhala wolungama kupambana Mulungu?
Kodi munthu angathe kukhala wangwiro kupambana Mlengi wake?
18 Ngati Mulungu sakhulupirira atumiki ake omwe,
ngati Iye amawapeza angelo ake ndi cholakwa,
19 nanga kuli bwanji ndi iwo amene amakhala m’nyumba zadothi,
amene maziko awo ndi fumbi,
amene amathudzuka mosavuta ngati kadziwotche!
20 Mmawa ali moyo, pofika madzulo afa;
mwakachetechete, amawonongeka kwamuyaya.
21 Kodi zonse zimene ali nazo sizimatheratu,
kotero kuti amafa osadziwa n’kanthu komwe?’

# 5

1 “Itana ngati ungathe, koma ndani adzakuyankhe?
Kodi ndi kwa mngelo uti ungapezeko thandizo?
2 Mkwiyo umapha chitsiru,
ndipo njiru imawononga wopusa.
3 Ine ndinaona chitsiru chitamera mizu,
koma mwadzidzidzi nyumba yake inatembereredwa.
4 Ana ake alibe ndi chitetezo chomwe;
amaponderezedwa m’bwalo la milandu popanda owateteza.
5 Anthu anjala amamudyera zokolola zake,
amamutengera ndi za pa minga pomwe,
ndipo anthu akhwinthi amafunkha chuma chake.
6 Pakuti masautso satuluka m’fumbi,
ndipo kuwukira sikuchokera m’dothi.
7 Komatu munthu amabadwira kuti azunzike
monga momwe mbaliwali zimathethekera mlengalenga.

8 “Koma ndikanakhala ine, ndikanamudandawulira Mulungu;
ndikanapereka mlandu wanga kwa Iye.
9 Iye amachita zozizwitsa zimene sizimvetsetseka,
zodabwitsa zimene sizingatheke kuwerengedwa.
10 Iye amagwetsa mvula pa dziko lapansi,
ndipo amathirira minda ya anthu.
11 Iye amakweza anthu wamba,
ndipo iwo amene akulira amawayika pa malo otetezedwa.
12 Iyeyo amalepheretsa chiwembu cha anthu ochenjera,
kotero kuti cholinga chawo sichipindula kanthu.
13 Iye amakola anthu ochenjera mu msampha wa kuchenjera kwawo,
ndipo zolinga za atambwali amazithetsa msangamsanga.
14 Mdima umawagwera nthawi yamasana;
nthawi yamasana amayenda moyambasayambasa monga nthawi ya usiku.
15 Mulungu amapulumutsa amphawi ku lupanga la m’kamwa mwawo;
amawapulumutsa m’manja mwa anthu amphamvu.
16 Choncho osauka ali ndi chiyembekezo,
ndipo anthu opanda chilungamo amawatseka pakamwa.

17 “Wodala munthu amene Mulungu amamudzudzula;

n'chifukwa chake usanyoze chilango cha Wamphamvuzonse.
18 Pakuti Iye amavulaza koma amamanganso mabalawo;
Iye amakantha munthu, komanso manja ake amachiritsa.
19 Pakuti adzakupulumutsa ku masautso nthawi ndi nthawi,
mavuto angachuluke bwanji, sadzakukhudza ndi pang'ono pomwe.
20 Pa nthawi ya njala adzakulanditsa ku imfa,
ndipo nthawi ya nkhondo adzakupulumutsa ku lupanga.
21 Adzakuteteza kwa anthu osinjirira,
ndipo palibe chifukwa chochitira mantha pamene chiwonongeko chafika.
22 Uzidzaseka pa nthawi ya chiwonongeko ndi ya njala,
ndipo palibe chifukwa chochitira mantha ndi zirombo za m'dziko lapansi.
23 Pakuti udzachita pangano ndi miyala ya m'munda mwako,
ndipo nyama zakuthengo zidzakhala nawe mwamtendere.
24 Udzadziwa kuti nyumba yako ndi malo otetezedwa;
udzawerengera katundu wako ndipo sudzapeza kanthu kamene kasowapo.
25 Udzadziwa kuti ana ako adzakhala ambiri,
ndipo zidzukulu zako zidzakhala ngati udzu wa m'dziko lapansi.
26 Udzafika ku manda utakalamba,
monga mitolo ya zokolola pa nyengo yake.

27 "Ife tafufuza zimenezi ndipo ndi zoona,
choncho uzimvere ndi kuzitsata."

# 6

*Mawu a Yobu*

1 Tsono Yobu anayankha kuti,
2 "Achikhala mavuto anga anayezedwa,
ndipo zipsinjo zanga zonse zikanayikidwa pa sikelo!
3 Ndithu, zikanalemera kupambana mchenga wa ku nyanja;
n'chifukwa chake mawu anga akhala okhadzula.
4 Mivi ya Wamphamvuzonse yandibaya,
thupi langa likumva ululu wa miviyo;
zoopsa za Mulungu zandizinga.
5 Kodi bulu wakuthengo amalira akakhala ndi msipu,
nanga ng'ombe imalira ikakhala ndi chakudya?
6 Kodi chakudya chosakoma n'kuchidya chopanda mchere,
nanga choyera cha dzira chimakoma?
7 Zakudya zimenezi sindifuna n'kuzilawa komwe;
zakudya zimenezi zimabwerera kukhosi.

8 "Aa, ndikanalandira chimene ndikuchipempha,
chikhala Mulungu anandipatsa chimene ndikuchiyembekezera,
9 achikhala chinamukomera Mulungu kuti anditswanye,
kulola dzanja lake kuti lindimenye ndi kundiwonongeratu!
10 Pamenepo ine ndikanakhalabe ndi chitonthozo ichi,
ndikanakondwa mu ululu wanga wosalekezawu
podziwa kuti sindinakane mawu a Woyerayo.

11 “Kodi mphamvu zanga n’zotani kuti ndizikhalabe ndi chiyembekezo?
Nanga zoyembekezera zanga n’zotani kuti ndipirirebe?
12 Kodi ine ndili ndi mphamvu?
Nanga thupi langa ndi lolimba ngati chitsulo?
13 Kodi ndili ndi mphamvu zodzithandizira ndekha,
nanga pakuti thandizo lachotsedwa kwa ine?

14 “Munthu amene ali kakasi ayenera kukhala ndi abwenzi odzipereka,
ngakhale kuti iyeyo wasiya kuopa Wamphamvuzonse.
15 Koma abale anga ndi wosadalirika ngati mitsinje yowuma msanga,
ngati mitsinje imene imathamanga.
16 Ali ngati mitsinje ya madzi akuda nthawi ya dzinja,
imene madzi ake amakhala ambiri chifukwa chakuchuluka kwa mvula,
17 koma madziwo amasiya kuyenda nthawi yachilimwe,
ndipo nthawi yotentha madziwo amawumiratu m’mitsinjemo.
18 Anthu oyenda pa ngamira amapatukirako kufuna madzi;
iwo amangoyendayenda n’kufera m’chipululu.
19 Anthu oyenda pa ngamira a ku Tema amafunafuna madzi,
anthu amalonda apaulendo a ku Seba amafunafuna mwa chiyembekezo.
20 Amataya mtima chifukwa ankayembekezera kupeza madzi;
koma akafika kumeneko, amangokhumudwako.
21 Tsono inunso mukuonetsa kuti ndinu osathandiza,
mukuona chinthu choopsa kwambiri ndipo mukuchita mantha.
22 Kodi ine ndinanenapo kuti, ‘Ndiperekereni kenakake,
ndilipirireni dipo kuchokera pa chuma chanu,
23 ndilanditseni m’dzanja la mdani,
ndiwomboleni m’dzanja la munthu wankhanza?’

24 “Phunzitseni, ndipo ine ndidzakhala chete;
ndionetseni pomwe ndalakwitsa.
25 Ndithu, mawu owona ndi opweteka!
Koma mawu anu otsutsa akufuna kuonetsa chiyani?
26 Kodi inu mukufuna kundidzudzula pa zimene ndikunena,
ndipo mukufuna kuyesa mawu a munthu wosweka mtima ngati mphepo chabe?
27 Inu mungathe kuchita maere kuti mugulitse ana amasiye
ndi kumugulitsa bwenzi lanu.

28 “Koma tsopano ndichitireni chifundo pamene mukundiyang’ana.
Kodi ine ndingayankhule zabodza pamaso panu?
29 Fewani mtima, musachite zosalungama;
ganiziraninso popeza chilungamo changa chikanalipobe.
30 Kodi pali choyipa chilichonse pa milomo yanga?
Kodi pakamwa panga sipangathe kuzindikira kanthu koyipa?

# 7

1 “Kodi munthu sakhala ndi ntchito yowawa pa dziko lapansi?
Kodi masiku ake sali ngati munthu waganyu?

2 Monga ngati kapolo wolakalaka mthunzi wa nthawi yamadzulo,
kapena ngati munthu waganyu woyembekezera malipiro ake,
3 choncho ine ndapatsidwa nthawi yongovutika pachabe,
ndiponso usiku wamasautso wapatsidwa kwa ine.
4 Ndikamagona ndimaganiza kuti, 'Kodi kucha liti?'
Usikuwo umatalika ndipo sindigona tulo mpaka mmawa.
5 Thupi langa ladzala mphutsi ndi zipsera,
khungu langa lang'ambika ndipo likutuluka mafinya.

6 "Masiku anga ndi othamanga kupambana makina wolukira nsalu,
ndipo amatha wopanda chiyembekezo.
7 Inu Mulungu kumbukirani kuti moyo wanga uli ngati mpweya;
sindidzaonanso masiku achisangalalo.
8 Amene akundiona tsopano akundiona;
mudzandifunafuna koma sindidzapezekanso.
9 Monga mtambo umazimirira ndi kukanganuka,
momwemonso munthu amene walowa m'manda sabwerera.
10 Iye sadzabweranso ku nyumba kwake
ndipo onse omudziwa adzamuyiwala.

11 "N'chifukwa chake ine sindidzakhala chete;
ndidzayankhula mopsinjika mtima,
ndidzadandaula mowawidwa mtima.
12 Kodi ine ndine nyanja kapena chirombo cham'nyanja
kuti inu mundiyikire alonda?
13 Pamene ndikuganiza kuti ndidzapeza chitonthozo pa bedi panga
ndipo pogona panga padzachepetsa madandawulo anga,
14 ngakhale nthawi imeneyo mumandiopseza ndi maloto
ndi kundichititsa mantha ndi masomphenya,
15 kotero kuti ndimalakalaka kudzikhweza kapena kufa,
kupambana kupirira zowawa zimene ndikuzimva m'thupi mwanga.
16 Ine ndatopa nawo moyo wanga; sindingakonde kukhala moyo nthawi zonse.
Ndisiyeni ndekha pakuti moyo wanga ulibe tanthauzo.

17 "Kodi munthu n'chiyani kuti muzimuganizira chotere,
kuti muzisamala zochita zake,
18 kuti muzimusanthula mmawa uliwonse
ndi kumamuyesa nthawi yonse?
19 Kodi simudzaleka kumandizonda
kuti ndipezeko mpata wopumula?
20 Ngati ine ndachimwa, ndachita chiyani kwa Inu,
Inu wopenyetsetsa anthu?
Chifukwa chiyani mwachititsa kuti ndikhale ngati choponyera chandamale chanu?
Kodi ndasanduka katundu wolemera kwa Inu?
21 Chifukwa chiyani simukundikhululukira zolakwa zanga
ndi kundichotsera machimo anga?
Pakuti posachedwa ndilowa m'manda;
mudzandifunafuna ine koma simudzandionanso."

# 8

*Mawu a Bilidadi*

1 Pamenepo Bilidadi wa ku Suki anayankha kuti,
2 “Kodi udzakhala ukuyankhula zoterezi mpaka liti?
Mawu ako ali ngati mphepo yamkuntho.
3 Kodi Mulungu amapotoza chiweruzo cholungama?
Kodi Wamphamvuzonse amalephera kuchita zachilungamo?
4 Pamene ana ako anamuchimwira Mulungu,
Iye anawapereka kuti alangidwe chifukwa cha tchimo lawo.
5 Koma utayang’ana kwa Mulungu,
ndi kudandaulira Wamphamvuzonse,
6 ngati uli wangwiro ndi wolungama mtima
ngakhale tsopano Iye adzachitapo kanthu m’malo mwako
ndipo adzakubwezeretsa pa malo ako oyenera.
7 Chiyambi chako chidzaoneka ngati chochepa
koma chimaliziro chako chidzakhala chopambana.

8 “Funsa kwa anthu amvulazakale
ndipo upeze zimene makolo awo anaziphunzira
9 pakuti ife ndife ana adzulodzuloli ndipo sitidziwa chilichonse,
ndipo moyo wathu pa dziko lapansi uli ngati chithunzithunzi.
10 Kodi iwo sadzakulangiza ndi kukufotokozera?
Kodi sadzakuwuza mawu ochokera pa zimene amazidziwa?
11 Kodi bango n’kumera pa nthaka yopanda chinyontho?
Nanga mawango n’kukula bwino popanda madzi?
12 Popanda madzi, zimenezi zimafota zikanali zaziwisi ndi zosadula;
zimawuma msangamsanga kuposa bango.
13 Ndimo mmene amachitira anthu onse amene amayiwala Mulungu;
ndi mmene chiyembekezo cha munthu wosapembedza Mulungu chimathera.
14 Kulimba mtima kwake kumafowoka;
zimene iye amadalira zili ngati ukonde wa kangawude.
15 Iye amatsamira ukonde wake, koma umaduka;
amawugwiritsitsa koma sulimba.
16 Munthu woyipayo ali ngati chomera chothiriridwa bwino chimene chili pa dzuwa,
nthambi zake zimatambalala pa munda wake;
17 mizu yake imayanga pa mulu wa miyala
ndi kufunafuna malo woti izikike pa miyalapo.
18 Koma pamene yachotsedwa pamalo pakepo,
pamalopo pamakana chomeracho ndi kuti, ‘Ine sindinakuonepo.’
19 Ndithudi chomeracho chimafota,
ndipo pa nthakapo pamatuluka zomera zina.

20 “Ndithudi, Mulungu sakana munthu amene alibe cholakwa
kapena kulimbikitsa anthu ochita zoyipa.
21 Iye adzadzaza m’kamwa mwako ndi phwete
ndipo milomo yako idzafuwula ndi chimwemwe.
22 Adani ako adzachita manyazi,
ndipo malo okhalamo anthu oyipa sadzaonekanso.”

# 9

### *Mawu a Yobu*

1 Ndipo Yobu anayankha kuti,
2 “Zoonadi, ndikudziwa kuti zimenezi ndi zoona.
Koma munthu angathe bwanji kukhala wolungama pamaso pa Mulungu?
3 Ngakhale wina atafuna kutsutsana naye,
Iye sangamuyankhe munthuyo ngakhale mawu amodzi omwe.
4 Mulungu ndi wa nzeru zambiri ndipo mphamvu zake ndi zochuluka.
Ndani analimbana naye popanda kupwetekeka?
5 Iye amasuntha mapiri, mapiriwo osadziwa,
ndipo amawagubuduza ali wokwiya.
6 Iye amagwedeza dziko lapansi kulisuntha pamalo pake
ndipo amanjenjemeretsa mizati yake.
7 Iye amayankhula ndi dzuwa ndipo siliwala;
Iyeyo amaphimba kuwala kwa nyenyezi.
8 Ndi Mulungu yekha amene anayala mayiko akumwamba
ndipo amayenda pa mafunde a pa nyanja.
9 Iye ndiye mlengi wa nyenyezi zamlalang’amba ndi akamwiniatsatana,
nsangwe ndi kumpotosimpita.
10 Iye amachita zozizwitsa zimene sizimvetsetseka,
zodabwitsa zimene sizingawerengeke.
11 Akapita pafupi ndi ine sindingathe kumuona;
akadutsa, sindingathe kumuzindikira.
12 Ngati Iye alanda zinthu, ndani angathe kumuletsa?
Ndani anganene kwa Iye kuti, ‘Mukuchita chiyani?’
13 Mulungu sabweza mkwiyo wake;
ngakhale gulu lankhondo la Rahabe linawerama pa mapazi ake.

14 “Nanga ine ndingathe kukangana naye bwanji?
Ndingawapeze kuti mawu oti n’kutsutsana naye?
15 Ngakhale nditakhala wosalakwa, sindingamuyankhe;
ndikanangopempha chifundo kwa woweruza wanga.
16 Ngakhale ndikanamuyitana ndipo Iye ndi kuvomera,
sindikhulupirira kuti akanamva mawu angawo.
17 Iye akanandikantha ndi mphepo yamkuntho,
ndipo akanandipweteka popanda chifukwa.
18 Mulungu sakanandilola kuti ndipumenso
koma akanandichulukitsira zowawa.
19 Tikanena za mphamvu, Iye ndi wamphamvudi!
Ndipo tikanena za chiweruzo cholungama, ndani angamuzenge mlandu?
20 Ngakhale ndikanakhala wosalakwa, zoyankhula zanga zikananditsutsa;
ndikanakhala wopanda cholakwa, pakamwa panga pakanandipeza wolakwa.

21 “Ngakhale ine ndili wosalakwa,
sindidziyenereza ndekha;
moyo wanga ndimawupeputsa.
22 Zonse n’zofanana; n’chifukwa chake ndikuti,
‘Iye amawononga anthu osalakwa ndi anthu oyipa omwe.’

23 Pamene mkwapulo ubweretsa imfa yadzidzidzi,
Iye amaseka tsoka la munthu wosalakwayo.
24 Pamene dziko lagwa m'manja mwa anthu oyipa
Iye amawatseka maso anthu oweruza dzikolo.
Ngati si Iyeyo, nanga ndani?

25 "Masiku anga ndi othamanga kwambiri kupambana munthu waliwiro;
masikuwo amapita ine osaonapo zabwino.
26 Amayenda ngati mabwato a njedza pa nyanja,
ngati mphungu zothamangira nyama zoti zidye.
27 N'tanena kuti, 'Ndidzayiwala madandawulo anga,
ndidzasintha nkhope yanga ndipo ndidzasekerera,'
28 ndikuopabe mavuto anga onse,
popeza ndikudziwa kuti simudzavomereza kuti ndine wosalakwa.
29 Popeza ndapezeka kale wolakwa
ndivutikirenji popanda phindu?
30 Ngakhale nditasamba m'madzi oyera kwambiri
ndi kusamba m'manja mwanga ndi sopo,
31 mutha kundiponyabe pa dzala,
kotero kuti ngakhale zovala zanga zomwe zidzandinyansa.

32 "Mulungu si munthu ngati ine kuti ndithe kumuyankha,
sindingathe kutsutsana naye m'bwalo la milandu.
33 Pakanapezeka munthu wina kuti akhale m'khalapakati wathu,
kuti atibweretse ife tonse pamodzi,
34 munthu wina woti achotse ndodo ya Mulungu pa ine
kuti kuopsa kwake kusandichititsenso mantha!
35 Pamenepo ine ndikanatha kuyankhula mosamuopa Mulunguyo,
koma monga zililimu, sindingathe.

# 10

1 "Ine ndatopa nawo moyo wanga;
choncho ndidzanena zodandaula zanga momasuka
ndipo ndidzayankhula mwa kuwawidwa mtima kwanga.
2 Ndidzati kwa Mulungu wanga: Musandiweruze kuti ndine wolakwa,
koma mundiwuze chifukwa chimene Inu mukukanganira ndi ine.
3 Kodi mumakondwera mukamandizunza,
kunyoza ntchito ya manja anu,
chonsecho mukusekerera ndi zochita za anthu oyipa?
4 Kodi maso anu ali ngati a munthu?
Kodi mumaona zinthu monga momwe amazionera munthu?
5 Kodi masiku anu ali ngati masiku a munthu,
kapena zaka zanu ngati zaka za munthu,
6 kuti Inu mufufuze zolakwa zanga
ndi kulondola tchimo langa,
7 ngakhale mukudziwa kuti sindine wolakwa
ndiponso kuti palibe amene angandilanditse m'dzanja lanu?

8 "Munandiwumba ndi kundipanga ndi manja anu.
Kodi tsopano Inu mudzatembenuka ndi kundiwononga?

9 Kumbukirani kuti munandipanga ndi dothi,
kodi tsopano mundibwezeranso ku fumbi?
10 Suja munapatsa abambo anga mphamvu zoti andibale,
suja munandikuza bwino m'mimba mwa amayi anga?
11 Munandikuta ndi khungu ndi mnofu
ndi kundilumikiza pamodzi ndi mafupa ndi mitsempha?
12 Munandipatsa moyo ndi kundionetsa chifundo chanu,
ndipo munasamalira bwino moyo wanga.

13 "Koma izi ndi zimene munabisa mu mtima mwanu,
ndipo ndikudziwa kuti zinali m'maganizo anu:
14 Kuti ngati ndingachimwe mudzakhala mukundipenyetsetsa
ndipo kuti simudzalola kuti ndisalangidwe chifukwa cha kulakwa kwanga.
15 Ngati ndili wolakwa, tsoka langa!
Koma ngakhale ndili wosalakwa sindingathe kutukula mutu wanga,
pakuti ndagwidwa ndi manyazi
ndipo ndamizidwa m'mavuto anga.
16 Ndipo ndikatukula mutu wanga, Inu mumandisaka ngati mkango
ndiponso mumandiopseza ndi mphamvu yanu.
17 Mumabweretsa mboni zatsopano potsutsana nane
ndipo mkwiyo wanu pa ine umanka nukulirakulira ndi
magulu anu olimbana nane amanka nachulukirachulukira.

18 "Chifukwa chiyani Inu munalola kuti ndibadwe?
Ndi bwino ndikanafa diso lililonse lisanandione.
19 Ndikanapanda kubadwa,
kapena akanangonditenga nditabadwa kupita nane ku manda!
20 Kodi masiku anga owerengeka sali pafupi kutha?
Ndilekeni kuti ndipumule pang'ono pokha
21 ndisanapite ku malo amene munthu sabwererako
ku dziko la imfa ndi kwa mdima wandiweyani,
22 ku dziko la mdima wandiweyani
ndi chisokonezo,
kumene kuwala kumakhala ngati mdima."

# 11

*Mawu a Zofari*

1 Pamenepo Zofari wa ku Naama anayankha kuti,
2 "Kodi mawu ambirimbiriwa n'kukhala osayankhidwa?
Kodi munthu woyankhulayankhulayu n'kulungamitsidwa?
3 Kodi anthu n'kukhala chete atamva kubwebweta kwakoku?
Kodi palibe wina amene adzakudzudzule pamene ukuyankhula zonyoza?
4 Iwe ukunena kwa Mulungu kuti, 'Zikhulupiriro zanga ndi zopanda zolakwika
ndipo ndine wangwiro pamaso panu.'
5 Aa, n'kanakonda Mulungu akanayankhula
kuti Iye atsekule pakamwa pake kutsutsana nawe
6 ndi kukuwululira chinsinsi cha nzeru yake,
pakuti nzeru yeniyeni ili ndi mbali ziwiri.

Dziwa izi: Mulungu wayiwala machimo ako ena.

7 “Kodi iwe ungathe kumvetsa zinsinsi za Mulungu?
Kodi ungafufuze malire a nzeru za Wamphamvuzonse?
8 Zili kutali kupambana mayiko akumwamba, nanga ungachite chiyani?
Ndi zakuya kupambana kuya kwa manda, nanga ungadziwe chiyani?
9 Muyeso wa nzeru zake ndi wautali kupambana dziko lapansi
ndipo ndi wopingasa kupambana nyanja.

10 “Ngati Iye atabwera ndi kukutsekera m’ndende
nakutengera ku bwalo la milandu, ndani angathe kumuletsa?
11 Ndithudi, Mulungu amazindikira anthu achinyengo;
akaona choyipa, kodi sachizindikira?
12 Munthu wopanda nzeru sizingatheke kukhala wanzeru
monganso mwana wa bulu wakuthengo sangasanduke munthu.

13 “Koma ngati upereka mtima wako kwa Iye
ndi kutambasulira manja ako kwa Iyeyo,
14 ngati utaya tchimo limene lili m’dzanja lako
ndi kusalola choyipa kuti chikhale m’moyo mwako,
15 udzatukula mutu wako wosachita manyazi;
udzayima chilili ndipo sudzachita mantha.
16 Udzayiwala ndithu zowawa zako,
zidzakhala ngati madzi amene apita kale.
17 Moyo wako udzawala kupambana usana,
ndipo mdima udzakhala ngati mmawa.
18 Udzalimba mtima popeza pali chiyembekezo;
ndipo udzayang’ana mbali zonse ndi kugona mosatekeseka.
19 Udzagona pansi, popanda wina wokuopseza
ndipo ambiri adzakupempha kuti uwachitire chifundo.
20 Koma anthu oyipa adzafuna thandizo osalipeza,
ndipo adzasowa njira yothawirapo;
chiyembekezo chawo chidzakhala imfa basi.”

# 12

*Mawu a Yobu*

1 Pamenepo Yobu anayankha kuti,
2 “Ndithudi inuyo ndinu anthu
ndipo nzeru zanu zidzafera nanu pamodzi!
3 Koma inenso ndili nazo nzeru ngati inu;
ineyo sindine munthu wamba kwa inu.
Ndani amene sadziwa zonse zimene mwanenazi?

4 “Ndasanduka chinthu choseketsa kwa abwenzi anga,
ngakhale ndinkapemphera kwa Mulungu ndipo Iye ankandiyankha.
Ine ndasanduka chinthu chongoseketsa, ngakhale ndili wolungama ndi wosalakwa!
5 Anthu amene ali pabwino amanyoza anzawo amene ali pa tsoka.
Tsokalo limagwa pa amene wayamba kale kugwa.
6 Nyumba za anthu achifwamba zimakhala pa mtendere,
ndipo anthu amene amaputa Mulungu amakhala pabwino,

amene amanyamula milungu yawo m’manja.

7 “Koma funsa nyama zakuthengo ndipo zidzakuphunzitsa,
kapena mbalame zamumlengalenga ndipo zidzakuwuza;
8 kapena uyankhule ndi dziko lapansi ndipo lidzakuphunzitsa,
kapena ulole nsomba zam’nyanja kuti zikufotokozere.
9 Kodi mwa zonsezi ndi chiti chimene sichidziwa
kuti lachita zimenezi ndi dzanja la Yehova?
10 M’manja mwake ndi m’mene muli moyo wa cholengedwa chilichonse,
ndiponso moyo wa anthu a mitundu yonse.
11 Kodi khutu sindiye limene limamva mawu
monga mmene lilime limalawira chakudya?
12 Kodi nzeru sipezeka pakati pa anthu okalamba?
Kodi moyo wautali sumabweretsa nzeru zomvetsa zinthu?

13 “Kwa Mulungu ndiye kuli nzeru ndi mphamvu;
uphungu ndi kumvetsa zinthu ndi zake.
14 Chimene Iye wapasula palibe angachimangenso.
Akatsekera munthu m’ndende palibe angamutulutse.
15 Iyeyo akamanga mvula dziko limawuma;
akamasula mvulayo, madzi amasefukira pa dziko.
16 Kwa Iye kuli mphamvu ndi kupambana;
munthu wopusitsidwa ndiponso wopusitsa onse ali mu ulamuliro wake.
17 Iye amalanda aphungu nzeru zawo
ndipo amapusitsa oweruza.
18 Iye amachotsa zingwe zimene mafumu anawamanga nazo
ndipo amawamanga lamba m’chiwuno mwawo.
19 Iye amasocheretsa ansembe atawalanda nzeru zawo
ndipo amagonjetsa anthu amphamvu amene ndi okhazikika.
20 Iye amakhalitsa chete aphungu odalirika
ndipo amalanda chidziwitso cha anthu akuluakulu.
21 Iye amanyoza anthu otchuka
ndipo anthu anyonga amawatha mphamvu.
22 Iye amatulutsira poyera zinthu zozama za mu mdima
ndipo mdima wandiweyaniwo amawusandutsa kuwala.
23 Iye amakuza mitundu ya anthu ndipo amayiwononganso;
amachulukitsa mitundu ya anthu ndipo amayimwazanso.
24 Iye amalanda nzeru za atsogoleri a dziko lapansi;
amawayendetsa m’thengo mopanda njira.
25 Iwo amafufuzafufuza njira mu mdima wopanda chowunikira;
Iye amawayendetsa dzandidzandi ngati oledzera.

# 13

1 “Ndaziona ndi maso anga zonsezi,
ndazimva ndi makutu anga ndipo ndazimvetsa.
2 Zimene inu mukudziwa, inenso ndimazidziwa;
ineyo sindine munthu wamba kwa inu.
3 Koma ine ndikulakalaka nditayankhula ndi Wamphamvuzonse
ndi kukamba mlandu wanga ndi Mulungu.

4 Koma inu mukundipaka mabodza;
nonsenu ndinu asing'anga opanda phindu!
5 Achikhala munangokhala chete nonsenu!
Apo mukanachita zanzeru.
6 Tsopano imvani kudzikanira kwanga;
imvani kudandaula kwa pakamwa panga.
7 Kodi inu mudzayankhula moyipa kuyankhulira Mulungu?
Kodi mudzayankhulira Iyeyo mwachinyengo?
8 Kodi mudzaonetsa kuti Iyeyo ngokondera?
Kodi inu mudzamuteteza Mulungu pa mlandu wake?
9 Mulungu atayang'anitsitsa, inu n'kukupezani wosalakwa?
Kodi inu mungamunamize Iye monga momwe munganamizire munthu?
10 Ndithudi, Iye angathe kukudzudzulani
ngati muchita zokondera mseri.
11 Kodi ulemerero wake sungakuopseni?
Kodi kuopsa kwake sikungakuchititseni mantha?
12 Mawu anu anzeru ali ngati miyambi yopanda tanthauzo;
mawu anu odzitchinjirizira ali ngati mpanda wadothi.

13 "Khalani chete ndipo ndilekeni ndiyankhule;
tsono zimene zindichitikire zichitike.
14 Chifukwa chiyani ndikuyika moyo wanga pa chiswe
ndi kutengera m'manja moyo wangawu?
15 Ngakhale Iye andiphe, komabe ndidzamukhulupirira;
ndithu, ndidzafotokoza mlandu wanga pamaso pake.
16 Zoonadi, ichi ndiye chidzakhala chipulumutso changa
pakuti palibe munthu wosapembedza amene angafike pamaso pake!
17 Mvetserani mosamala mawu anga;
makutu anu amve zimene ndikunena.
18 Pakuti tsopano ndawukonzekera mlandu wanga,
ndikudziwa ndipo adzandipeza wolungama.
19 Kodi alipo wina amene angatsutsane nane?
ngati zili choncho, ndidzakhala chete ndi kufa.

20 "Inu Mulungu, ndipatseni zinthu ziwiri izi,
ndipo pamenepo ine sindidzakubisalirani:
21 Muchotse dzanja lanu pa ine,
ndipo muleke kundichititsa mantha ndi kuopsa kwanuko.
22 Tsono muyitane ndipo ndidzayankha,
kapena mulole kuti ine ndiyankhule ndipo Inu muyankhe.
23 Kodi zolakwa zanga ndi zingati ndipo machimo anga ndi angati?
Wonetseni kulakwa kwanga ndi machimo anga.
24 Chifukwa chiyani mukundifulatira
ndi kundiyesa ine mdani wanu?
25 Kodi mudzazunza tsamba lowuluka ndi mphepo?
Kodi mudzathamangitsa mungu wowuma?
26 Pakuti Inu mwalemba zinthu zowawa zonditsutsa nazo
ndipo mukundipaka machimo a pa ubwana wanga.
27 Inu mwamanga miyendo yanga ndi maunyolo.
Mumayang'anitsitsa mayendedwe anga onse

poyika zizindikiro pamene mapazi anga apondapo.

28 “Motero munthu amatha ngati chinthu chofumbwa,
ngati chovala chodyedwa ndi njenjete.

# 14

1 “Munthu wobadwa mwa amayi
amakhala masiku owerengeka ndipo ndi odzaza ndi mavuto okhaokha.
2 Amaphuka ngati duwa ndipo kenaka amafota;
amathawa ngati mthunzi ndipo sakhalitsa.
3 Kodi munthu wotereyo n’kumuyang’anitsitsa?
Kodi mungamubweretse pamaso panu kuti mumuzenge mlandu?
4 Ndani angatulutse chabwino m’choyipa?
Palibe ndi mmodzi yemwe!
5 Masiku a munthu ndi odziwikiratu;
munakhazikitsa chiwerengero cha miyezi yake
ndipo munamulembera malire amene sangathe kuwalumpha.
6 Choncho Inu mumufulatire ndipo mumuleke apumule
kufikira atakondwera nawo moyo ngati munthu waganyu.

7 “Mtengo uli nacho chiyembekezo:
ngati wadulidwa, udzaphukiranso
ndipo nthambi zake sizidzaleka kuphukira.
8 Mizu yake ingathe kukalamba m’nthaka
ndipo chitsa chake n’kuwola pa dothi,
9 koma pamene chinyontho chafika udzaphukira
ndipo udzaphuka nthambi ngati mtengo wanthete.
10 Koma munthu amafa nayikidwa m’manda,
amapuma mpweya wotsiriza ndipo kutha kwake n’komweko.
11 Monga madzi amaphwera m’nyanja
kapena monga mtsinje umaphwera nuwuma,
12 momwemonso munthu amagona ndipo sadzukanso;
mpaka zamlengalenga zidzathe, anthu sadzauka
kapena kudzutsidwa ku tulo tawo.

13 “Aa, Inu mukanangondibisa m’manda
ndi kundiphimba kuti ndisaoneke mpaka mkwiyo wanu utapita!
Achikhala munandiyikira nthawi,
kuti pambuyo pake mundikumbukirenso.
14 Munthu akafa, kodi adzakhalanso ndi moyo?
Masiku anga onse a moyo wovutikawu
ndidzadikira mpaka itafika nthawi yomasulidwa.
15 Inu mudzandiyitane ndipo ndidzakuyankhani;
inu mudzafunitsitsa kuona cholengedwa chimene munachipanga ndi manja anu.
16 Ndithudi pamenepo mudzayang’ana mayendedwe anga
koma simudzalondola tchimo langa.
17 Zolakwa zanga zidzakulungidwa m’thumba;
inu mudzaphimba tchimo langa.

18 “Koma monga phiri limakokolokera ndi kuswekasweka
ndipo monga thanthwe limasunthira kuchoka pa malo ake,
19 monganso madzi oyenda amaperesera miyala
ndipo madzi othamanga amakokololera nthaka,
momwemonso Inu mumawononga chiyembekezo cha munthu.
20 Inu mumamugonjetsa kamodzin’kamodzi ndipo munthuyo n’kutheratu;
Inu mumasintha maonekedwe a nkhope yake ndipo mumamutaya kutali.
21 Ana ake akamalemekezedwa, iyeyo sazidziwa zimenezo;
akamachititsidwa manyazi iye saziona zimenezo.
22 Iye amangomva zowawa za m’thupi lake
ndipo amangodzilirira yekha mwini wakeyo.”

# 15

*Mawu a Elifazi*

1 Pamenepo Elifazi wa ku Temani anayankha kuti,
2 “Kodi munthu wanzeru angayankhe ndi mawu achabechabe otere,
kapena angakhutitse mimba yake ndi mphepo yotentha yochokera kummawa?
3 Kodi angathe kutsutsa ndi mawu opanda pake,
kapena kuyankhula mawu opanda phindu?
4 Koma iwe ukuchepetsa zoopa Mulungu
ndipo ukutchinga zodzikhuthulira kwa Mulungu.
5 Tchimo lako ndiye likuyankhulitsa pakamwa pakopo;
ndipo watengera mayankhulidwe a atambwali.
6 Pakamwa pakopo ndiye pakukutsutsa osati pakamwa panga;
milomo yakoyo ikukutsutsa.

7 “Kodi ndiwe munthu woyamba kubadwa?
Kodi unalengedwa mapiri asanalengedwe?
8 Kodi unali m’gulu la alangizi a Mulungu?
Kodi ukudziyesa wanzeru ndiwe wekha?
9 Kodi iwe umadziwa chiyani chimene ife sitichidziwa?
Kodi iwe uli ndi chidziwitso chanji chimene ife tilibe?
10 Anthu a imvi ndi okalamba ali mbali yathu,
anthu amvulazakale kupambana abambo ako.
11 Kodi mawu otonthoza mtima ochokera kwa Mulungu sakukukwanira,
mawu oyankhula mofatsawa kwa iwe?
12 Chifukwa chiyani ukupsa mtima,
ndipo chifukwa chiyani ukutuzula maso ako,
13 moti ukupsera mtima Mulungu
ndi kuyankhula mawu otero pakamwa pako?

14 “Kodi munthu n’chiyani kuti n’kukhala woyera mtima
kapena wobadwa mwa amayi n’chiyani kuti n’kukhala wolungama mtima?
15 Ngati Mulungu sakhulupirira ngakhale angelo ake,
ngakhale zakumwamba sizoyera pamaso pake,
16 nanga kuli bwanji munthu amene ndi wonyansa ndi wa njira zokhotakhota,
amene kuchita zoyipa kuli ngati kumwa madzi.

17 “Mvetsera kwa ine ndipo ndidzakufotokozera;
ndilole ndikuwuze zimene ndaziona,
18 zimene anandiphunzitsa anthu anzeru,
sanandibisire kalikonse kamene anamva kuchokera kwa makolo awo.
19 (Ndi kwa iwowa kumene dziko lino linaperekedwa
pamene panalibe mlendo wokhala pakati pawo).
20 Munthu woyipa amavutika ndi masautso masiku onse a moyo wake,
munthu wankhanza adzavutika zaka zake zonse.
21 Amamva mawu owopsa m’makutu mwake,
pamene zonse zikuoneka ngati zili bwino, anthu achifwamba amamuthira nkhondo.
22 Iye sakhulupirira kuti angathe kupulumuka ku mdima wa imfa;
iyeyo ndi woyenera kuphedwa.
23 Amangoyendayenda pali ponse kunka nafuna chakudya;
amadziwa kuti tsiku la mdima lili pafupi.
24 Masautso ndi nthumanzi zimamuchititsa mantha kwambiri;
zimamugonjetsa iye monga imachitira mfumu yokonzekera kukathira nkhondo,
25 chifukwa iye amatambasula dzanja lake kuyambana ndi Mulungu
ndipo amadzitama yekha polimbana ndi Wamphamvuzonse.
26 Amapita mwa mwano kukalimbana naye
atanyamula chishango chochindikala ndi cholimba.

27 “Ngakhale nkhope yake ndi yonenepa
ndipo m’chiwuno mwake muli mnofu wambiri,
28 munthuyo adzakhala m’mizinda yowonongeka
ndi m’nyumba zosayenera kukhalamo anthu,
nyumba zimene zikugwa ndi kuwonongeka.
29 Iye sadzalemeranso ndipo chuma chake sichidzakhalitsa,
ngakhale minda yake sidzabala zipatso pa dziko lapansi.
30 Iyeyo sadzapulumuka mu mdimamo;
lawi lamoto lidzawumitsa nthambi zake,
ndipo mpweya wochokera m’kamwa mwa Mulungu udzamusesa.
31 Asadzinyenge yekha podalira zinthu zachabechabe,
pakuti pa mapeto pake sadzaphulapo kanthu.
32 Iye adzalandira malipiro ake nthawi yake isanakwane,
ndipo nthambi zake sizidzaphukanso.
33 Iye adzakhala ngati mtengo wamphesa wopululidwa zipatso zake zisanapse,
adzakhala ngati mtengo wa olivi umene wayoyola maluwa ake.
34 Pakuti anthu osapembedza Mulungu adzakhala osabala
ndipo moto udzapsereza nyumba za onse okonda ziphuphu.
35 Iwo amalingalira zaupandu ndipo amachita zoyipa;
mtima wawo umakonzekera zachinyengo.”

# 16

*Mawu a Yobu*

1 Pamenepo Yobu anayankha kuti,
2 “Ndinamvapo zambiri monga zimenezi;
nonsenu ndinu anthu osatha kutonthoza mtima mnzanu.
3 Kodi mawu anu ochulukawo adzatha?

Kodi chikukuvutani n'chiyani kuti muzingoyankhula mawu otsutsawa?
4 Inenso ndikanatha kuyankhula monga inu,
inuyo mukanakhala monga ndilili inemu;
Ine ndikanatha kuyankhula mawu omveka bwino kutsutsana nanu
ndi kukupukusirani mutu wanga.
5 Ndipo mawu a pakamwa panga akanakulimbikitsani;
chitonthozo chochokera pa milomo yanga chikanachepetsa ululu wanu.

6 "Koma ine ndikati ndiyankhule ululu wanga sukuchepa;
ndipo ndikati ndikhale chete, ululu wanga sukuchokabe.
7 Ndithudi, Inu Mulungu mwanditha mphamvu;
mwawononga banja langa lonse.
8 Inu mwandimanga ndipo kundimangako kwakhala umboni;
kuwonda kwanga kwandiwukira ndipo kukuchita umboni wonditsutsa.
9 Mulungu amabwera kwa ine mwankhanza ndipo amadana nane,
amachita kulumira mano;
mdani wanga amandituzulira maso.
10 Anthu amatsekula pakamwa pawo kundikuwiza;
amandimenya pa tsaya mwachipongwe
ndipo amagwirizana polimbana nane.
11 Mulungu wandipereka kwa anthu ochita zoyipa
ndipo wandiponyera m'manja mwa anthu oyipa mtima.
12 Ine ndinali pamtendere, koma Mulungu ananditswanya;
anandigwira pa khosi ndi kundiphwanya.
Iye anandisandutsa choponyera chandamale chake;
13 anthu ake oponya mauta andizungulira.
Mopanda kundimvera chisoni, Iye akulasa impsyo zanga
ndipo akutayira pansi ndulu yanga.
14 Akundivulaza kawirikawiri,
akuthamangira pa ine monga munthu wankhondo.

15 "Ndasokerera chiguduli pa thupi langa
ndipo ndayika mphamvu zanga pa fumbi.
16 Maso anga afiira ndi kulira,
ndipo zikope zanga zatupa;
17 komatu manja anga sanachite zachiwawa
ndipo pemphero langa ndi lolungama.

18 "Iwe dziko lapansi, usakwirire magazi anga;
kulira kwanga kofuna thandizo kusalekeke!
19 Ngakhale tsopano mboni yanga ili kumwamba;
wonditchinjiriza pa mlandu wanga ali komweko.
20 Wondipembedzera ndi bwenzi langa,
pamene maso anga akukhuthula misozi kwa Mulungu;
21 iye, m'malo mwanga, amamudandaulira Mulungu
monga munthu amadandaulira bwenzi lake.

22 "Pakuti sipapita zaka zambiri
ndisanayende m'njira imene sindidzabwerera."

## 17

1 "Mtima wanga wasweka,
masiku anga atha,
manda akundidikira.
2 Ndithudi, anthu ondiseka andizungulira;
maso anga akupenyetsetsa mdani wanga.

3 "Inu Mulungu, patseni chikole chimene mukufuna.
Ndani wina amene adzandiperekera ine chikole?
4 Inu mwatseka maganizo awo kuti asamvetse zinthu;
choncho simudzawalola kuti apambane.
5 Ngati munthu apereka mnzake chifukwa cha chuma,
ana ake sadzaona mwayi.

6 "Mulungu wandisandutsa chisudzo chochiseka aliyense,
munthu amene anthu amalavulira malovu nkhope yake.
7 M'maso mwanga mwada ndi chisoni;
ndawonda ndi mutu womwe.
8 Anthu olungama akudabwa nazo zimenezi;
anthu osachimwa akupsera mtima anthu osapembedza Mulungu.
9 Komabe anthu olungama adzasunga njira zawo,
ndipo anthu a makhalidwe abwino mphamvu zawo zidzanka zikuchu-
luka.

10 "Tsono bwerani nonsenu, bwerezaninso mawu anuwo,
sindidzapezapo munthu wanzeru pakati panupo.
11 Masiku anga atha, zimene ndinakonza zalephereka,
pamodzinso ndi zokhumba za mtima wanga.
12 Anthu awa amasandutsa usiku kukhala usana,
nthawi ya usiku iwo amati 'kwatsala pang'ono kucha.'
13 Ngati nyumba imene ndikuyiyembekezera ndi manda,
ngati ndiyala bedi langa mu mdima,
14 ngati ndinena kwa dzenje la manda 'ndinu abambo anga,'
ndiponso kwa mphutsi kuti, 'ndinu amayi anga' kapena 'mlongo
wanga,'
15 tsono chiyembekezo changa chili kuti?
Ndani angaone populumukira panga?
16 Ndithu sindidzakhalanso ndi chiyembekezo chilichonse,
polowa m'manda, pamene ndidzatsikira ku fumbi."

## 18

*Mawu a Bilidadi*

1 Pamenepo Bilidadi wa ku Suki anayankha kuti,
2 "Kodi iwe Yobu utsiriza liti zoyankhula zakozi?
Khala munthu wozindikira zinthu ndipo ukatero ife tidzayankhula.
3 Chifukwa chiyani ukutiyesa ngati ng'ombe
ndi kuoneka ngati opusa m'maso mwako?
4 Iwe amene ukudzipweteka wekha ndi mkwiyo wako,
kodi dziko lapansi lisanduke bwinja chifukwa cha iweyo?
Kodi kapena thanthwe lisunthidwe kuchoka pa malo ake?

5 “Nyale ya munthu woyipa yazimitsidwa;
malawi a moto wake sakuwalanso.
6 Kuwala kwa m’nyumba mwake kwasanduka mdima;
nyale ya pambali pake yazima.
7 Mayendedwe ake amgugu azilala;
fundo zake zomwe zamugwetsa.
8 Mapazi ake amulowetsa mu ukonde
ndipo akungoyendayenda mu ukondewo.
9 Msampha wamkola mwendo;
khwekhwe lamugwiritsitsa.
10 Amutchera msampha pansi mobisika;
atchera diwa pa njira yake.
11 Zoopsa zikumuchititsa mantha kumbali zonse,
zikutsatira mayendedwe ake onse.
12 Mphamvu zake zatha chifukwa cha njala,
tsoka likumudikira.
13 Wagwidwa nthenda yoopsa thupi lonse;
miyendo yake, manja ake, zonse zawola.
14 Wachotsedwa m’nyumba imene ankadalira,
ndipo amukokera ku imfa, mfumu ya zoopsa zonse.
15 M’nyumba mwake zonse zachotsedwamo;
awazamo sulufule kuti aphe tizirombo ta matenda.
16 Mizu yake ikuwuma pansi
ndipo nthambi zake zikufota
17 Sadzakumbukiridwanso pa dziko lapansi;
sadzakhalanso ndi chinthu chomutchukitsa m’dziko.
18 Amuchotsa pa malo owala ndi kumuponya ku mdima,
ndipo amupirikitsa pa dziko lonse.
19 Iye alibe ana kapena zidzukulu pakati pa anthu ake,
kulibe wotsala kumene iye ankakhala.
20 Anthu akumadzulo adabwa kwambiri ndi tsoka lake;
anthu akummawa agwidwa ndi mantha aakulu.
21 Ndithudi, izi ndiye zimagwera munthu woyipa;
amenewa ndiye mathero a munthu amene sadziwa Mulungu.”

# 19

### *Mawu a Yobu*

1 Pamenepo Yobu anayankha kuti,
2 “Kodi mudzakhala mukundizunza mpaka liti,
ndi kundilasa ndi mawu anuwo?
3 Inuyo mwandinyoza kwambiri;
mwanditsutsa mopanda manyazi.
4 Ngati ndi zoona kuti ine ndasochera,
cholakwachotu n’changa.
5 Ngati ndithudi mukudziyika nokha pamwamba panga,
ndi kugwiritsa ntchito kunyozedwa kwanga polimbana nane,
6 pamenepa dziwani kuti Mulungu wandilakwira
ndipo wandizinga ukonde wake.

7 “Ngakhale ndifuwule kuti, ‘Akundizunza!’ Palibe wondiyankha;
ngakhale ndipemphe thandizo, palibe wondichitira zolungama.

8 Mulungu wanditsekera njira yanga kotero sindingathe kudutsa;
waphimba njira zanga ndi mdima.
9 Iye wandilanda ulemu wanga
ndipo wandivula chipewa chaufumu pamutu panga.
10 Wandiphwanyaphwanya mbali zonse ndipo ndatheratu;
Iye wazula chiyembekezo changa ngati mtengo.
11 Wandikwiyira ndipo
akundiyesa mmodzi mwa adani ake.
12 Ankhondo ake akubwera kwa ine mwamphamvu,
akonzekera zodzalimbana nane
ndipo azungulira nyumba yanga.

13 "Mulungu wandisiyanitsa ndi abale anga;
wasandutsa odziwana nane kukhala achilendo kwa ine.
14 Abale anga andithawa;
abwenzi anga andiyiwala.
15 Anthu odzacheza ku nyumba kwanga ndiponso antchito anga aakazi andisandutsa mlendo;
ndasanduka mlendo m'maso mwawo.
16 Ndikayitana wa ntchito wanga, iye sandiyankha,
ngakhale ndikapempha ndi pakamwa panga sandichitira kanthu.
17 Mpweya wanga umamunyansa mkazi wanga;
ndine chinthu chonyansa kwa abale anga a mimba imodzi.
18 Inde, ngakhale ana amandinyoza;
akandiona amandinyodola.
19 Anzanga onse apamtima amanyansidwa nane;
iwo amene ndinkawakonda andiwukira.
20 Ndangotsala khungu ndi mafupa okhaokha;
ndapulumuka lokumbakumba.

21 "Mvereni chisoni, inu abwenzi anga, mvereni chisoni,
pakuti dzanja la Mulungu landikantha.
22 Chifukwa chiyani mukundilondola ngati Mulungu?
Kodi simunatope nalo thupi langa?

23 "Aa, achikhala mawu anga analembedwa,
achikhala analembedwa m'buku,
24 akanalembedwa pa mwala ndi chitsulo,
akanalembedwa pa thanthwe kuti sangathe kufufutidwa!
25 Koma ndikudziwa kuti mpulumutsi wanga ali ndi moyo,
ndipo pa nthawi yomaliza adzabwera kudzanditeteza.
26 Ndipo khungu langa litatha n'kuwonongeka,
m'thupi langa lomweli ndidzamuona Mulungu.
27 Ine ndemwe ndidzamuona Iye
ndi maso angawa, ineyo, osati wina ayi.
Ndithu mtima wanga ukufunitsitsadi!

28 "Koma inu mukuti, 'Haa! Tingamuzunze bwanji,
popeza kuti zonsezi zaoneka chifukwa cha iye yemweyo?'
29 Inu muyenera kuopa lupanga;
pakuti mkwiyo wake umalangadi ndi lupanga;
zikadzatero muzadziwa kuti chiweruzo chilipo ndithu."

# 20

*Mawu a Zofari*

1 Pamenepo Zofari wa ku Naama anayankha kuti
2 “Kuvutika kwa m’maganizo kwanga kwandifulumiza kuti ndiyankhe
chifukwa ndasautsidwa kwambiri.
3 Ndikumva kudzudzula kondinyoza,
ndipo kumvetsetsa kwanga kwa zinthu kwandifulumiza kuti ndiyankhe.

4 “Ndithudi iwe ukudziwa momwe zinthu zakhala zikuchitikira kuyambira kale,
kuchoka nthawi imene munthu analengedwa pa dziko lapansi,
5 kuti chisangalalo cha woyipa n’chosachedwa kutha,
chimwemwe cha wosapembedza Mulungu n’chakanthawi kochepa.
6 Ngakhale atamayenda mapewa ake ali mmwamba
ndipo mutu wake uli neng’aa,
7 iye adzatheratu monga momwe imatayikira ndowe yake yomwe;
iwo amene ankamuona adzati, ‘Kodi uje uja ali kuti?’
8 Adzazimirira ngati maloto ndipo sadzapezekanso,
adzachotsedwa ngati masomphenya a usiku.
9 Diso limene linamuona silidzamuonanso;
sadzapezekanso pamalo pake.
10 Ana ake adzabwezera zonse
zimene iyeyo analanda anthu osauka;
11 Mphamvu zaunyamata zimene zili m’thupi mwake
zidzagona naye limodzi m’fumbi.

12 “Ngakhale zoyipa zili zozuna m’kamwa mwake
ndipo amazibisa kunsi kwa lilime lake,
13 ngakhale salola kuzilavula,
ndipo amazisunga m’kamwa mwake,
14 koma chakudya chake chidzawawasa m’mimba mwake;
chidzasanduka ngati ndulu ya njoka m’kati mwa iyeyo.
15 Adzachisanza chuma chimene anachimeza;
Mulungu adzachitulutsa m’mimba mwa munthuyo.
16 Iye adzayamwa ndulu ya njoka ndipo
ululu wa mphiri udzamupha.
17 Sadzasangalala ndi timitsinje,
mitsinje yoyenda uchi ndi mafuta.
18 Ayenera kubweza zimene anazigwirira ntchito osazidya;
sadzasangalala ndi phindu la malonda ake.
19 Pakuti iye anapondereza anthu osauka ndipo anawasiya wopanda thandizo;
iyeyo analanda nyumba zimene sanamange.

20 “Chifukwa choti umbombo wake sutha,
sadzatha kusunga chilichonse chimene amakondwera nacho.
21 Palibe chatsala kuti iye adye;
chuma chake sichidzachedwa kutha.
22 Ngakhale ndi munthu wachuma, mavuto adzamugwera;
mavuto aakulu adzamugwera.

23 Akadya n'kukhuta,
Mulungu adzamugwetsera ukali wamoto
ngati mvula yosalekeza.
24 Ngakhale athawe mkondo wachitsulo,
muvi wamkuwa wosongoka udzamulasa.
25 Muviwo adzawutulutsira ku msana,
songa yake yowala kuchoka m'mphafa mwake.
Adzagwidwa ndi mantha aakulu;
26 mdima wandiweyani ukudikira chuma chake.
Moto wopanda wowukoleza udzamupsereza
ndi kuwononga zonse zotsala m'nyumba yake.
27 Zamumlengalenga zidzawulula kulakwa kwake;
dziko lapansi lidzamuwukira.
28 Chigumula cha madzi chidzawononga nyumba yake,
katundu wake adzatengedwa pa tsiku la ukali wa Mulungu.
29 Izi ndi zimene Mulungu amasungira anthu oyipa,
mphotho imene Mulungu amayikira iwowo."

# 21

*Mawu a Yobu*

1 Pamenepo Yobu anayankha kuti,
2 "Mvetserani bwino mawu anga;
ichi chikhale chitonthozo changa chochokera kwa inu.
3 Ndiloleni ndiyankhule
ndipo ndikatha kuyankhula munditonzetonze.

4 "Kodi ine ndikudandaulira munthu?
Tsono ndilekerenji kupsa mtima?
5 Ndipenyeni ndipo mudabwe;
mugwire dzanja pakamwa.
6 Ndikamaganiza zimenezi ndimachita mantha kwambiri;
thupi langa limanjenjemera.
7 Chifukwa chiyani anthu oyipa amakhalabe ndi moyo,
amakalamba ndi kusanduka amphamvu?
8 Amaona ana awo akukhazikika pamodzi nawo,
zidzukulu zawo zikukula bwino iwo akuona.
9 Mabanja awo amakhala pa mtendere ndipo sakhala ndi mantha;
mkwapulo wa Mulungu suwakhudza n'komwe.
10 Ng'ombe zawo zazimuna sizilephera kubereketsa;
ng'ombe zawo zazikazi sizipoloza.
11 Amatulutsa ana awo ngati gulu la nkhosa;
makanda awo amavinavina pabwalo.
12 Amayimba nyimbo pogwiritsa ntchito matambolini ndi azeze;
amakondwa pakumva kulira kwa chitoliro.
13 Zaka zawo zimatha ali mu ulemerero
ndipo amatsikira ku manda mwamtendere.
14 Koma anthuwo amawuza Mulungu kuti, 'Tichokereni!'
Ife tilibe chikhumbokhumbo chofuna kudziwa njira zanu.
15 Kodi Wamphamvuzonseyo ndani kuti timutumikire?
Ife tipindula chiyani tikamapemphera kwa Iyeyo?
16 Komatu ulemerero wawo suli m'manja mwawo,

koma ine ndimakhala patali ndi uphungu wa anthu oyipa.

17 “Koma n’kangati kamene nyale ya anthu oyipa imazimitsidwa?
N’kangati kamene tsoka limawagwera?
N’kangati kamene Mulungu amawakwiyira ndi kuwalanga?
18 N’kangati kamene iwo amakhala ngati phesi lowuluka ndi mphepo,
ngati mungu wowuluzika ndi kamvuluvulu?
19 Paja amati, ‘Mulungu amalanga ana chifukwa cha machimo abambo awo.’
Koma Mulungu amabwezera chilango munthuyo, kuti adziwe kuti Mulungu amalangadi.
20 Mulole kuti adzionere yekha chilango chake,
kuti alawe ukali wa Wamphamvuzonse.
21 Nanga kodi amalabadira chiyani zabanja lake limene walisiya m’mbuyo,
pamene chiwerengero cha masiku ake chatha?

22 “Kodi alipo wina amene angaphunzitse Mulungu nzeru,
poti Iye amaweruza ngakhale anthu apamwamba?
23 Munthu wina amamwalira ali ndi mphamvu zonse,
ali pa mtendere ndi pa mpumulo,
24 thupi lake lili lonenepa,
mafupa ake ali odzaza ndi mafuta.
25 Munthu wina amamwalira ali wowawidwa mtima,
wosalawapo chinthu chabwino chilichonse.
26 Olemera ndi osauka omwe amamwalira ndi kuyikidwa m’manda
ndipo onse amatuluka mphutsi.

27 “Ndikudziwa bwino zimene mukuganiza,
ziwembu zanu zomwe mukuti mundichitire.
28 Inu mukuti, ‘Kodi nyumba ya mkulu uja ili kuti,
matenti amene munkakhala anthu oyipa aja ali kuti?’
29 Kodi munawafunsapo anthu amene ali pa ulendo?
Kodi munaganizirapo zimene iwo amanena?
30 Zakuti munthu woyipa amasungidwa chifukwa cha tsiku la tsoka,
kuti amapulumutsidwa chifukwa cha tsiku la ukali wa Mulungu?
31 Kodi ndani amadzudzula munthu wochimwayo?
Ndani amamubwezera zoyipa zimene anachita?
32 Iye amanyamulidwa kupita ku manda
ndipo anthu amachezera pa manda ake.
33 Dothi la ku chigwa limamukomera;
anthu onse amatsatira mtembo wake,
ndipo anthu osawerengeka amakhala patsogolo pa chitanda chakecho.

34 “Nanga inu mudzanditonthoza bwanji ine ndi mawu anu opanda-pakewo
palibe chimene chatsala kuti muyankhe koma mabodza basi!”

# 22

*Mawu a Elifazi*

1 Pamenepo Elifazi wa ku Temani anayankha kuti,
2 “Kodi munthu n’kukhala waphindu kwa Mulungu?

Kodi munthu wanzeru angamupindulire Iye?
3 Kodi Wamphamvuzonse akanapeza chabwino chotani iweyo ukanakhala wolungama?
Kodi iyeyo akanapeza phindu lanji makhalidwe ako akanakhala angwiro?

4 “Kodi n’chifukwa choti umamuopa, kuti azikudzudzula,
kuti azifuna kukukokera ku mlandu?
5 Kodi osati n’chifukwa chakuti kuyipa kwako n’kwakukulu?
Kodi machimo ako si opanda malire?
6 Iwe unkawumiriza abale ako kuti akupatse chikole popanda chifukwa;
umalanda anthu zovala zawo ndi kuwasiya amaliseche.
7 Sunawapatse madzi anthu otopa,
ndipo unawamana chakudya anthu anjala,
8 ngakhale unali munthu wamphamvu, wokhala ndi malo akeake,
munthu waulemu wake, wokhala m’dzikomo.
9 Ndipo akazi amasiye unawachotsa wopanda kanthu,
ndipo unapondereza ana amasiye.
10 N’chifukwa chake misampha yakuzungulira,
n’chifukwa chake tsoka ladzidzidzi lakuchititsa mantha,
11 n’chifukwa chake kuli mdima kuti sungathe kuona kanthu,
n’chifukwa chakenso madzi achigumula akumiza.

12 “Kodi Mulungu sali kutalitali kumwamba?
Ndipo ona nyenyezi zili mmwamba kwambirizo, ona kutalika kwake pamene zililipo!
13 Komabe iweyo ukunena kuti, ‘Kodi Mulungu amadziwa chiyani?
Kodi Iye amaweruza mu mdima woterewu?
14 Mitambo yakuda yamuphimba, kotero kuti Iye sakutiona
pamene akuyendayenda pamwamba pa thambopo.’
15 Kodi iwe udzayendabe m’njira yakale
imene anthu oyipa ankayendamo?
16 Iwo anachotsedwa nthawi yawo isanakwane,
maziko awo anakokoloka ndi madzi achigumula.
17 Anthuwo anati kwa Mulungu, ‘Tichokereni!
Kodi Wamphamvuzonse angatichitire chiyani?’
18 Chonsecho ndi Iye amene anadzaza nyumba zawo ndi zinthu zabwino,
choncho ine sindigwirizana ndi uphungu wa anthu oyipa.

19 “Anthu olungama amaona kuwonongeka kwawo ndipo amakondwera;
anthu osalakwa amangoseka, akamuona woyipa akulangidwa.
20 Amanena kuti, ‘Ndithudi adani athu awonongeka
ndipo moto wawononga chuma chawo!’

21 “Gonjera Mulungu kuti ukhale naye pamtendere;
ukatero udzaona zabwino.
22 Landira malangizo a pakamwa pake
ndipo usunge mawu ake mu mtima mwako.
23 Ukabwerera kwa Wamphamvuzonse udzabwezeretsedwa;
ukachotsa zoyipa zonse zimene zimachitika m’nyumba mwako,
24 ndipo chuma chamtengowapatali nuchiona ngati fumbi,

golide wa ku Ofiri numutaya ku miyala ya ku zigwa.
25 Pamenepo Wamphamvuzonseyo adzakhala golide wako,
siliva wako wamtengowapatali.
26 Pamenepo udzakondwera naye Wamphamvuzonse
ndipo udzakweza nkhope yako kwa Mulungu.
27 Udzamupempha ndipo adzakumvera,
ndipo udzapereka zimene unalonjeza.
28 Chimene watsimikiza kuti uchite, chidzachitikadi,
kuwala kudzakuwunikira pa njira yako.
29 Pamene anthu agwetsedwa pansi, iwe n'kunena kuti, 'Akwezeni!'
Pamenepo Iye adzapulumutsa anthu oponderezedwa.
30 Iye adzapulumutsa ngakhale munthu amene ndi wolakwa,
ameneyo adzapulumutsidwa kudzera m'kulungama kwako."

# 23

*Yobu*

1 Pamenepo Yobu anayankha kuti,
2 "Leronso kudandaula kwanga n'kwakukulu kwambiri;
Iye akundilanga kwambiri ngakhale ndi kubuwula.
3 Ndikanangodziwa kumene ndikanamupeza Mulungu;
ndikanangopita kumene amakhalako!
4 Ndikanafotokoza mlandu wanga pamaso pake
ndipo ndikanayankhula mawu odziteteza.
5 Ndikanadziwa mawu amene Iye akanandiyankha,
ndi kulingalira bwino zimene akananena!
6 Kodi Iye akanalimbana nane mwa mphamvu zake zazikulu?
Ayi, Iye sakanayankhula zinthu zotsutsana nane.
7 Kumeneko munthu wolungama akanafotokoza mlandu wake pamaso pake,
ndipo woweruzayo akanandipeza wosalakwa nthawi zonse.

8 "Taonani, ndikapita kummawa, Iye kulibe kumeneko,
ndikapita kumadzulo sinditha kumupeza kumeneko.
9 Akamagwira ntchito kumpoto, sindimuona kumeneko
akapita kummwera, sindimuona.
10 Koma Iye amadziwa mmene ndimayendera;
Iyeyo akandiyesa adzandipeza kuti ndili ngati golide.
11 Mapazi anga akhala akuponda m'mapazi ake;
ndasunga njira yake ndipo sindinayitaye.
12 Sindinapatuke kusiya malamulo ochokera pakamwa pake;
ndasunga mawu a pakamwa pake kupambana chakudya changa cha tsiku ndi tsiku.

13 "Koma Iyeyo ndi wosasinthika, ndipo ndani angatsutsane naye?
Iye amachita chilichonse chimene wafuna.
14 Iye amachita chimene watsimikiza kuti chindichitikire,
ndipo malingaliro oterowa ali nawobe.
15 N'chifukwa chake ndikuchita mantha kwambiri pamaso pake;
ndikamaganiza zonsezi ndimamuopa.
16 Mulungu walefula mtima wanga;
Wamphamvuzonse wandiopseza kwambiri.

17 Komatu sindinachititsidwe mantha ndi mdima,
ndi mdima wandiweyani umene waphimba nkhope yanga.

# 24

1 “Chifukwa chiyani Wamphamvuzonse sayikiratu nthawi yoti aweruze?
Chifukwa chiyani iwo amene amadziwa Iyeyo amayembekezera pachabe masiku oterewa?
2 Anthu amasuntha miyala ya m’malire, kuti akuze dziko lawo;
amadyetsa ziweto zimene aba.
3 Amalanda abulu a ana amasiye
ndipo amatenganso ng’ombe ya mkazi wamasiye ngati chikole.
4 Amachotsa m’misewu anthu osauka,
ndipo amathamangitsa amphawi onse m’dziko.
5 Amphawiwo amakhala ngati mbidzi m’chipululu,
amayendayenda kufuna chakudya;
dziko lowuma limapereka chakudya cha ana awo.
6 Iwo amakolola za m’minda ya eni ake,
ndipo amakunkha mphesa m’minda ya anthu oyipa.
7 Amagona maliseche usiku wonse kusowa zovala;
pa nthawi yozizira amasowa chofunda.
8 Amavumbwa ndi mvula ya m’mapiri
ndipo amakangamira ku matanthwe kusowa pobisalapo.
9 Amatsomphola mwana wamasiye wa ku bere;
ndipo amagwira mwana wakhanda wa m’mphawi kuti akhale chikole.
10 Amphawi amangoyenda maliseche kusowa zovala;
amasenza mitolo ya tirigu, koma n’kumagonabe ndi njala.
11 Iwo amayenga mafuta a olivi m’minda ya anthu oyipa;
amapsinya mphesa, koma n’kumamvabe ludzu.
12 Kubuwula kwa anthu amene akufa kumamveka kuchokera mu mzinda,
anthu ovulala akulirira chithandizo.
Koma Mulungu sakuyimba mlandu wina aliyense.

13 “Pali ena amene amakana kuwala,
amene safuna kuyenda m’kuwalako
kapena kukhala m’njira zake.
14 Dzuwa likalowa, wopha anzake amadzuka
ndipo amakapha osauka ndi amphawi;
nthawi ya usiku iye amasanduka mbala.
15 Munthu wachigololo amadikira chisisira;
iyeyo amaganiza kuti, ‘Palibe amene akundiona,’
ndipo amaphimba nkhope yake.
16 Mbala zimathyola nyumba usiku,
koma masana zimadzitsekera;
izo zimathawa kuwala.
17 Pakuti kwa onsewa mdima wandiweyani ndiye kuti kwawachera.
Iwo amachita ubale ndi zoopsa za mdima.

18 “Komatu iwowo ndi thovu loyandama pa madzi;
minda yawo ndi yotembereredwa pa dzikolo
kotero kuti palibe amene amapita ku minda ya mpesa.
19 Monga momwe kutentha ndi chilala zimasungunulira madzi owundana

ndi momwemonso mmene manda amachotsera omwe achimwa.
20 Mayi wowabereka amawayiwala,
mphutsi zimasangalala powadya;
anthu oyipa sakumbukiridwanso
koma amathyoka ngati mtengo.
21 Amachitira nkhanza mayi wosabala ndi mayi amene alibe mwana,
ndipo sakomera mtima mkazi wamasiye.
22 Koma Mulungu amawononga munthu wamphamvu mwa mphamvu zake;
ngakhale munthuyo atakhazikika, alibe chiyembekezo cha moyo wake.
23 Mulungu atha kuwalola kuti akhale mosatekeseka,
koma amakhala akupenyetsetsa njira zawo.
24 Kwa kanthawi kochepa oyipa amakwezedwa ndipo kenaka saonekanso;
amatsitsidwa ndipo amachotsedwa monga ena onse;
amadulidwa ngati ngala za tirigu.

25 "Ngati zimenezi sizoona, ndani angaonetse kuti ndine wabodza
ndi kusandutsa mawu anga kukhala wopanda pake?"

# 25

*Mawu a Bilidadi*

1 Apo Bilidadi wa ku Suki anayankha kuti,
2 "Ulamuliro ndi kuopsa ndi za Mulungu,
Iye amakhazikitsa bata mu ufumu wake kumwambako.
3 Kodi magulu ake ankhondo n'kuwerengeka?
Kodi kuwala kwake sikuwalira ndani?
4 Kodi munthu angakhale bwanji wolungama pamaso pa Mulungu?
Kodi munthu wobadwa mwa mayi angakhale wangwiro?
5 Ngati mwezi sutha kuwala kwenikweni,
ndipo nyenyezi sizitha kuwala pamaso pake,
6 nanji tsono munthu amene ali ngati mphutsi,
mwana wa munthu amene ali ngati nyongolotsi!"

# 26

*Mawu a Yobu*

1 Pamenepo Yobu anayankha kuti,
2 "Wamuthandizadi munthu wopanda mphamvu!
Walimbitsadi dzanja la munthu wofowoka!
3 Wapereka malangizo kwa munthu amene alibe nzeru!
Ndipotu waonetsadi nzeru zochuluka!
4 Kodi wakuthandiza ndani kuti uyankhule mawu awa?
Ndipo ndi mzimu wa yani umene unayankhula pakamwa pako?

5 "Mizimu ya anthu akufa ikunjenjemera pansi pa madzi,
ndi zonse zokhala m'madzimo.
6 Dziko la anthu akufa ndi lapululu pamaso pa Mulungu;
chiwonongeko ndi chosaphimbidwa.
7 Mulungu anayala thambo la kumpoto pa phompho;
Iye anakoloweka dziko lapansi m'malo mwake pamene panali popanda n'kanthu komwe.

8 Amasunga madzi ambiri m'mitambo yake,
koma mitamboyo siphulika chifukwa cha kulemera kwa madziwo.
9 Iye amaphimba mwezi wowala,
amawuphimba ndi mitambo yake.
10 Mulungu anawalembera madzi malire wonga uta,
kukhala malire pakati pa kuwunika ndi mdima.
11 Mizati yochirikiza mitambo yakumwamba imanjenjemera,
ndi kudabwa pa kudzudzula kwake.
12 Ndi mphamvu zake anatontholetsa nyanja;
ndi nzeru zake anakantha chirombo cha m'madzi chija chotchedwa Rahabe.
13 Ndi mpweya wake anayeretsa zamumlengalenga,
dzanja lake linapha chinjoka chothawa chija.
14 Zimenezi ndi pang'ono chabe mwa ntchito yake;
tingomva pang'ono za Iye ngati kunong'ona!
Kodi ndani angathe kudziwa kukula kwa mphamvu zake?"

# 27

1 Ndipo Yobu anapitiriza kuyankhula kwake:
2 "Ndithu pali Mulungu wamoyo, amene wakana kundiweruza molungama,
Wamphamvuzonse, amene wawawitsa mtima wanga,
3 nthawi zonse pamene ndili ndi moyo,
mpweya wa Mulungu uli m'mphuno mwanga,
4 pakamwa panga sipadzatuluka mawu oyipa,
lilime langa silidzayankhula zachinyengo.
5 Sindidzavomereza kuti inu mukunena zoona;
mpaka imfa yanga, sindidzataya ungwiro wanga.
6 Ndidzasunga chilungamo changa ndipo sindidzalola kuti chindichokere;
chikumbumtima changa sichidzanditsutsa nthawi yonse ya moyo wanga.

7 "Mdani wanga akhale ngati woyipa,
wondiwukira akhale ngati munthu wosalungama!
8 Nanga chiyembekezo cha munthu wosapembedza n'chiyani pamene aphedwa,
pamene Mulungu achotsa moyo wake?
9 Kodi Mulungu amamva kulira kwake
pamene zovuta zamugwera?
10 Kodi adzapeza chikondwerero mwa Wamphamvuzonse?
Kodi adzapemphera kwa Mulungu nthawi zonse?

11 "Ndidzakuphunzitsani za mphamvu ya Mulungu ndipo
sindidzabisa njira za Wamphamvuzonse.
12 Inu mwadzionera nokha zonsezi.
Nanga bwanji mukuyankhula zopanda pake?

13 "Pano pali chilango chimene Mulungu amasungira woyipa,
cholowa chimene munthu wankhanza amalandira kuchokera kwa Wamphamvuzonse.
14 Angakhale ana ake achuluke chotani adzaphedwa ndi lupanga ndipo
zidzukulu zake zidzasowa zakudya.

15 Amene adzatsalireko adzafa ndi mliri,
ndipo akazi awo amasiye sadzawalira.
16 Ngakhale aunjike siliva ngati fumbi,
ndi kukundika zovala ngati mchenga,
17 zimene wasungazo wolungama ndiye adzavale,
ndipo anthu osalakwa ndiwo adzagawane siliva wakeyo.
18 Nyumba imene akuyimanga ili ngati mokhala kadziwotche,
ili ngati msasa umene mlonda amamanga.
19 Amapita kokagona ali wolemera koma kutha kwake n'komweko;
akatsekula maso ake, chuma chake chonse chapita.
20 Zoopsa zimamukokolola ngati madzi achigumula;
mphepo yamkuntho imamunyamula usiku.
21 Mphepo ya kummawa imamuwulutsa ndipo iye saonekanso ndipo
imamuchotsa pamalo pake.
22 Imakuntha pa iye osamuchitira chisoni,
pamene akuyesa kuthawa mphamvu zake mwaliwiro.
23 Mphepoyo imamuwomba ndithu
ndipo kuchokera pamalo pake imamuopseza."

# 28

1 Pali mgodi wa siliva
ndiponso malo oyengerapo golide.
2 Chitsulo amachikumba pansi,
ndipo mkuwa amawusungunula ku miyala yamkuwa.
3 Munthu amalowa mu mdima atatenga nyale,
amafunafuna miyala mpaka ku malire a mgodiwo,
kufuna mkuwa mu mdima wandiweyani.
4 Amakumba njira zapansi mu mgodimo, kutali ndi kumene kumakhala anthu,
kumalo kumene phazi la munthu silinapondeko;
iye amakhala ali lende pansipo namazungulira uku ndi uku.
5 Nthaka, imene imatulutsa zakudya,
kunsi kwake kumachita ngati kwasandulizika ndi moto;
6 miyala ya safiro imachokera m'matanthwe ake,
ndipo m'fumbi lake mumakhala miyala yagolide.
7 Palibe mbalame yodya zinzake imene imadziwa njira yobisikayi,
palibe kamtema amene anayiona.
8 Zirombo zolusa sizipondamo m'njiramo,
ndipo mkango sudzeranso m'menemo.
9 Munthu amaphwanya matanthwe olimba,
ndipo amagubuduza mapiri kuyambira m'tsinde.
10 Amabowola njira m'matanthwewo;
ndipo amaona chuma chonse cha m'phirimo.
11 Amaletsa mitsinje ya pansipo kuti isayendenso,
motero amatulutsira poyera zinthu zobisika.

12 "Koma nzeru zingapezeke kuti?
Kodi kumvetsa zinthu kumakhala kuti?
13 Munthu sadziwa kufunika kwake kwa nzeruzo;
nzeruyo sipezeka pa dziko lino la anthu amoyo.
14 Phompho likuti, 'Sizipezeka mwa ine muno.'

Nyanja ikuti, ‘Mwa ine munonso ayi.’
15 Nzeru sungazigule ndi golide wabwino kwambiri,
mtengo wake sungawuyerekeze ndi siliva wambiri.
16 Nzeru singagulidwe ndi golide wa ku Ofiri,
kapena ndi miyala ya onikisi kapena ya safiro.
17 Nzeru sungayiyerekeze ndi golide kapena mwala wa galasi,
sungayigule ndi zokometsera zagolide.
18 Miyala ya korali ndi krisitali siyoyeneranso ndi kuyitchula n’komwe;
mtengo wa nzeru ndi woposa miyala ya rubi.
19 Nzeru sungayiyerekeze ndi miyala ya topazi ya ku Kusi;
nzeru singagulidwe ndi golide wabwino kwambiri.

20 “Kodi tsono nzeru zimachokera kuti?
Kodi kumvetsa zinthu kumakhala kuti?
21 Malo ake ndi obisika kwa zamoyo zonse,
ndi obisika ngakhale kwa mbalame zamlengalenga.
22 Chiwonongeko ndi imfa zikuti,
‘Tangomva mphekesera chabe ya zimenezo!’
23 Mulungu yekha ndiye amadziwa njira yake yopita kumeneko,
ndipo Iye yekha amadziwa kumene nzeru imakhala,
24 pakuti Iye amayang’ana mpaka ku malekezero a dziko lapansi
ndipo amaona zonse za kunsi kwa thambo.
25 Iye atapatsa mphepo mphamvu zake,
nayeza kuzama kwa nyanja,
26 atakhazikitsa lamulo loti mvula izigwa
ndi kukonza njira ya ching’aning’ani cha bingu,
27 pamenepo ndi pamene anayang’ana nzeruzo naziyeza mtengo wake;
nazikhazikitsa ndi kuzisanthula bwino lomwe.
28 Ndipo Iye anati kwa munthu,
‘Taonani, kuopa Ambuye, ndiye nzeru zimenezo
ndipo kuthawa zoyipa ndiye kumvetsa zinthu kumeneko.’ ”

# 29

1 Yobu anapitiriza kuyankhula kwake:
2 “Aa! Ndikanakhala momwe ndinalili miyezi yapitayi,
masiku amene Mulungu ankandiyang’anira,
3 pamene nyale yake inkandiwunikira
ndipo ndi kuwunika kwakeko ine ndinkatha kuyenda mu mdima!
4 Ndithu, masiku amene ndinali pabwino kwambiri,
pamene ubwenzi wa Mulungu unkabweretsa madalitso pa nyumba yanga,
5 nthawi imene Wamphamvuzonse anali nane,
ndipo ana anga anali atandizungulira m’mbalimu,
6 pamene popondapo ine panali patakhathamira mafuta a mkaka,
ndipo pa thanthwe pamatuluka mitsinje ya mafuta a olivi.

7 “Pamene ndinkapita pa chipata cha mzinda
ndi kukhala pa mpando wanga pabwalo,
8 anyamata amati akandiona ankapatuka
ndipo anthu akuluakulu ankayimirira;
9 atsogoleri ankakhala chete

ndipo ankagwira pakamwa pawo;
10 anthu otchuka ankangoti duu,
ndipo malilime awo anali atamatirira ku nkhama zawo.
11 Aliyense amene anamva za ine anayankhula zabwino zanga,
ndipo iwo amene anandiona ankandiyamikira,
12 chifukwa ndinkapulumutsa m'mphawi wofuna chithandizo,
ndiponso mwana wamasiye amene analibe aliyense womuthandiza.
13 Munthu amene anali pafupi kufa ankandidalitsa;
ndinkasangalatsanso mkazi wamasiye.
14 Chilungamo chinali ngati chovala changa;
chiweruzo cholungama ndiye chinali mkanjo ndi nduwira yanga.
15 Ndinali ngati maso kwa anthu osapenya;
ndinali ngati mapazi kwa anthu olumala.
16 Ndinali ngati abambo kwa anthu aumphawi;
ndinkayimira mlendo pa mlandu wake.
17 Ndinkawononga mphamvu za anthu oyipa
ndi kulanditsa amene anali atagwidwa.

18 "Ndinkaganiza kuti, 'Ndidzafera m'nyumba yanga,
masiku a moyo wanga ali ochuluka ngati mchenga.
19 Mizu yanga idzatambalalira ku madzi,
ndipo mame adzakhala pa nthambi zanga usiku wonse.
20 Ulemerero wanga udzakhala wosaguga mwa ine,
ndipo uta wanga udzakhala watsopano nthawi zonse m'dzanja langa.'

21 "Anthu ankamvetsera zimene ndinkanena mwachidwi,
ankadikira atakhala chete kuti amve malangizo anga.
22 Ndikayankhula, iwo sankayankhulanso;
mawu anga ankawagwira mtima.
23 Ankayembekezera ine monga momwe amayembekezera mvula
ndipo ankalandira mawu anga ngati mvula ya m'malimwe.
24 Ndikawasekerera, iwo sankatha kukhulupirira;
kuwala kwa nkhope yanga chinali chinthu chamtengowapatali kwa iwowo.
25 Ndinkawasankhira njira yawo ndipo ndinkawatsogolera ngati mfumu;
ndinkakhala ngati mfumu pakati pa gulu lake lankhondo;
ndinali ngati msangalatsi pakati pa anthu olira."

## 30

1 "Koma tsopano akundinyoza,
ana ang'onoang'ono kwa ine,
anthu amene makolo awo sindikanawalola
kuti azithandizana ndi agalu anga kuweta nkhosa zanga.
2 Kodi mphamvu zawo ndi za phindu lanji kwa ine,
pakuti mphamvu zawo zinatha kale?
3 Anali atatheratu kuwonda ndi njala,
ankayendayenda m'dziko lopanda madzi,
m'chipululu usiku.
4 Ankathyola therere ndi masamba owawa,
ndipo chakudya chawo chinali mizu ya mitengo ya masache.
5 Anapirikitsidwa pakati pa anthu anzawo,

akuwakuwiza ngati kuti anali akuba.
6 Anawumirizidwa kukhala ku zigwembe za mitsinje yowuma,
pakati pa matanthwe ndi m'maenje a m'nthaka.
7 Ankalira ngati nyama kuthengo
ndipo ankawunjikana pamodzi pa ziyangoyango.
8 Anali anthu achabechabe ndi wopanda dzina,
anathamangitsidwa m'dziko.

9 "Ndipo tsopano ana awo akundiyimba nyimbo zachipongwe;
ineyo ndasanduka chisudzo chawo.
10 Iwo amanyansidwa nane ndipo amandithawa;
akandiona salephera kundilavulira m'maso mwangamu.
11 Tsopano pakuti Mulungu wakhwefula uta wanga ndipo wandisautsa,
iwowo analekeratu kundiopa.
12 Ku dzanja langa lamanja anthu akulimbana nane;
andikumbira dzenje loti ndigweremo ndikamayenda,
andipangira mitumbira ya nkhondo kuti alimbane nane.
13 Iwo anditsekera njira;
akufuna kundichititsa ngozi,
popanda wina aliyense wowaletsa.
14 Akundithamangitsa ngati madzi olowera pa mpanda wobowoka,
iwo akubwererabwerera pakati pa chipasupasu.
15 Zoopsa zandithetsa mphamvu;
ulemu wanga wachita ngati wauluzika ndi mphepo,
chuma changa chija chazimirira ngati mtambo.

16 "Ndipo tsopano mtima wanga wachokamo;
ndili m'masiku amasautso.
17 Mafupa anga akuphwanya usiku pakuti
zowawa zanga sizikuleka.
18 M'mphamvu zake Mulungu wakhala ngati chovala changa;
Iye wandigwira ngati chovala chondithina pa khosi.
19 Wandiponya m'matope,
ndipo ndasanduka ngati fumbi ndi phulusa.

20 "Inu Mulungu, ine ndikulirira kwa Inu, koma simukundiyankha;
ndikayimirira, Inu simundiyang'ana n'komwe.
21 Inuyo mumandichitira zankhanza;
mumandizunza ndi dzanja lanu lamphamvu.
22 Mwandinyamulira ku mphepo ndipo mwandiwulutsa ndi mphepoyo;
mwandiponya m'mphepo ya mkuntho.
23 Ndikudziwa kuti Inu mudzandifikitsa ku imfa,
kumalo kumene amoyo onse adzapitako.

24 "Ndithudi palibe munthu amene amalanga munthu wosweka mtima,
amene akupempha thandizo m'masautso ake.
25 Kodi ine sindinalire nawo iwo amene anali pamavuto?
Kodi mtima wanga sunamvere chisoni anthu osauka?
26 Koma pamene ndinkayembekezera zabwino, zoyipa ndiye zinandigwera;
pamene ndinkafunafuna kuwala, mdima ndiye unandigwera.

27 Kuwawa kwa m'kati mwanga sikukuleka;
ndili m'masiku amasautso.
28 Ndikuyenda wothimbirira, komatu osati ndi dzuwa;
ndimayimirira pa msonkhano ndi kupempha chithandizo molira.
29 Ndasanduka m'bale wa nkhandwe,
mnzawo wa akadzidzi.
30 Khungu langa layamba kuda ndipo likufunduka;
thupi langa likutentha chifukwa cha kuphwanya kwa thupi.
31 Pangwe wanga wasanduka woyimbira maliro,
ndipo chitoliro changa chikuyimbira anthu olira.

# 31

1 "Ndinachita pangano ndi maso anga
kuti sindidzapenya namwali momusirira.
2 Kodi Mulungu kumwambako wandisungira zotani?
Kodi cholowa changa chochokera kwa Wamphamvuzonse kumwambako n'chotani?
3 Kodi si chiwonongeko kwa anthu oyipa,
tsoka kwa iwo amene amachita zolakwa?
4 Kodi Mulungu saona zochita zanga,
ndi kudziwa mayendedwe anga?

5 "Ngati ndachita zinthu mwachiphamaso,
kapena kufulumira kukachita zachinyengo,
6 Mulungu andiyeze ndi muyeso wake wolungama
ndipo Iye adzadziwa kuti ine ndine wosalakwa,
7 ngati mayendedwe anga asempha njira,
ngati mtima wanga wakhumbira zimene maso anga aona,
kapena ngati ndachita choyipa chilichonse.
8 Pamenepo ena adye zimene ndinadzala,
ndipo zomera zanga zizulidwe.

9 "Ngati mtima wanga unakopekapo ndi mkazi,
ndipo ngati ndinalakalaka mkazi wa mnansi wanga,
10 pamenepo mkazi wanga aphikire mwamuna wina chakudya,
ndipo amuna ena azigona naye.
11 Pakuti zimenezo zikanakhala zochititsa manyazi,
tchimo loyenera kulangidwa nalo.
12 Ndi moto umene umayaka mpaka chiwonongeko;
ukanapsereza zokolola zanga.

13 "Ngati ndinkapondereza mlandu wa akapolo anga aamuna kapena aakazi,
pamene ankabwera kwa ine ndi milandu yawo,
14 ndidzatani pamene Mulungu adzanditsutsa?
Nanga ndidzayankha chiyani akadzandifunsa?
15 Kodi amene anapanga ine m'mimba mwa amayi anga si yemwe anapanganso iwo?
Kodi si mmodzi yemweyo amene anatipanga tonsefe m'mimba mwa amayi athu?

16 “Ngati ndinawamana aumphawi zinthu zimene ankazikhumba,
kapena kuwagwiritsa fuwa lamoto akazi amasiye amene amafuna thandizo kwa ine,
17 ngati chakudya changa ndinadya ndekha,
wosagawirako mwana wamasiye,
18 chonsechotu kuyambira unyamata wanga ndinamulera monga abambo ake,
ndipo moyo wanga wonse ndakhala ndikusamalira akazi amasiye,
19 ngati ndinaona wina aliyense akuzunzika ndi usiwa,
kapena munthu wosauka alibe chofunda,
20 ndipo ngati iyeyo sananditamandepo
chifukwa chomufunditsa ndi nsalu ya ubweya wankhosa,
21 ngati ndinaopsezapo mwana wamasiye,
poganiza kuti ndinali ndi mphamvu m’bwalo la milandu,
22 pamenepo phewa langa lipokonyeke,
mkono wanga ukonyoke polumikizira pake.
23 Popeza ine ndinaopa kwambiri chiwonongeko chochokera kwa Mulungu,
ndinachitanso mantha ndi ulemerero wake, sindikanatha kuchita zinthu zimenezi.

24 “Ngati ndinayika mtima wanga pa chuma
kapena kunena kwa golide wabwino kwambiri kuti, ‘Iwe ndiye chitetezo changa,’
25 ngati ndinakondwera chifukwa choti chuma changa chinali chambiri,
zinthu zimene manja anga anazipeza,
26 ngati pamene ndinaona dzuwa likuwala,
kapena mwezi ukuyenda mwa ulemerero wake,
27 ndipo kuti mtima wanga unakopeka nazo
n’kuyika dzanja langa pakamwa mozilemekeza,
28 pamenepo zimenezinso zikanakhala machimo oti ndilangidwe nawo,
chifukwa ndikanakhala wosakhulupirika kwa Mulungu wakumwamba.

29 “Ngati ndinasangalala ndi kuwonongeka kwa mdani wanga,
kapena kusekera mavuto pamene mavuto anamugwera,
30 ine sindinachimwe ndi pakamwa panga
potulutsa matemberero a mdani wanga kuti awonongeke,
31 ngati anthu amene ndimakhala nawo m’nyumba mwanga sananenepo kuti,
‘Kodi ndani amene sakhuta ndi chakudya cha Yobu?’
32 Komatu mlendo sindinamusiye pa msewu usiku wonse,
pakuti khomo langa linali lotsekuka nthawi zonse kwa alendo,
33 ngati ndinabisa tchimo langa monga amachitira anthu ena,
kubisa kulakwa mu mtima mwanga
34 chifukwa choopa gulu la anthu,
ndi kuchita mantha ndi mnyozo wa mafuko
kotero ndinakhala chete ndipo sindinatuluke panja.

35 “Aa, pakanakhala wina wondimva!
Tsopano ndikutsiriza mawu anga odzitetezera. Wamphamvuzonse andiyankhe;

mdani wanga achite kulemba pa kalata mawu ake ondineneza.
36 Ndithu ine ndikanakoleka kalatayo pa phewa langa,
ndikanayivala kumutu ngati chipewa chaufumu.
37 Ndikanamufotokozera zonse zimene ndinachita;
ndikanafika pamaso pake ngati kalonga.

38 “Ngati minda yanga ikulira monditsutsa ine
ndipo malo ake onse osalimidwa anyowa ndi misozi,
39 ngati ndinadya za m’minda mwake osapereka ndalama
kapena kukhumudwitsa anthu olima m’mindamo,
40 pamenepo m’mindamo mumere namsongole m’malo mwa tirigu
ndi udzu m’malo mwa barele.”
Mawu a Yobu athera pano.

# 32

*Mawu a Elihu*

1 Tsono anthu atatuwa analeka kumuyankha Yobu, chifukwa chakuti
iyeyo ankadziona kuti ndi wolungama. 2 Koma Elihu, mwana wa Barakeli,
wa fuko la Buzi, wa banja la Ramu, anapsera mtima kwambiri Yobu
chifukwa choti Yobuyo anakana kuvomera kuti anachimwa ndi kuti
Mulungu anakhoza pomulanga. 3 Anapseranso mtima abwenzi ake atatu
aja chifukwa sanapeze njira yomutsutsira Yobu, ngakhale iwo anamupeza
kuti anali wolakwa. 4 Tsono Elihu anadikira kuti ayankhule ndi Yobu
chifukwa choti abwenziwo anali akuluakulu kupambana iyeyo. 5 Koma
Elihu ataona kuti anthu atatuwo analibe mawu oti ayankhulenso, iye
anapsa mtima.

6 Choncho Elihu mwana wa Barakeli wa fuko la Buzi anati:
“Ine ndine wamng’ono,
inuyo ndinu akuluakulu,
n’chifukwa chake ndimaopa,
ndimachita mantha kuti ndikuwuzeni zimene ndimadziwa.
7 Ndimaganiza kuti, ‘Ayambe ndi akuluakulu kuyankhula;
anthu amvulazakale ndiwo amaphunzitsa nzeru.’
8 Koma mzimu wa Mulungu mwa munthu,
mpweya wa Wamphamvuzonse, ndi umene umapereka nzeru zomvetsa zinthu.
9 Si okalamba amene ali ndi nzeru,
si amvulazakale okha amene ali ndi nzeru zomvetsa zinthu zimene zili zoyenera.

10 “N’chifukwa chake ndikuti, ‘Mvereni;
inenso ndikukuwuzani zimene ndikuzidziwa.’
11 Ndadikira nthawi yonseyi,
ndimamvetsera mwachidwi zimene mumayankhula,
pamene mumafunafuna mawu oti muyankhule,
12 ineyo ndinakumvetseranidi.
Koma palibe ndi mmodzi yemwe wa inu amene anatsutsa Yobu;
palibe aliyense wa inu amene anamuyankha mawu ake.
13 Musanene kuti, ‘Ife tapeza nzeru;
Mulungu ndiye amutsutse, osati munthu.’
14 Koma Yobu sanayankhule motsutsana ndi ine,

ndipo ine sindimuyankha monga mmene inu mwamuyankhira.

15 “Iwo asokonezeka ndipo alibe choti ayankhulenso;
mawu awathera.
16 Kodi ine ndidikire chifukwa iwo sakuyankhula tsopano,
pakuti angoyima phee wopanda yankho?
17 Inenso ndiyankhulapo tsopano;
nanenso ndinena zimene ndikudziwa.
18 Pakuti ndili nawo mawu ambiri,
ndipo mtima wanga ukundikakamiza;
19 m’kati mwanga ndili ngati botolo lodzaza ndi vinyo,
ngati matumba a vinyo watsopano amene ali pafupi kuphulika.
20 Ndiyenera kuyankhula kuti mtima utsike;
ndiyenera kutsekula pakamwa panga ndi kuyankha.
21 Sindidzakondera munthu wina aliyense,
kapena kuyankhula zoshashalika,
22 pakuti ndikanakhala wa luso loyankhula moshashalika,
Mlengi wanga akanandilanga msanga.”

# 33

1 “Koma tsopano, inu abambo Yobu chonde mverani mawu anga;
mutcherere khutu zonse zimene ndinene.
2 Tsopano ndiyamba kuyankhula;
mawu anga ali pa msonga ya lilime langa.
3 Mawu anga akuchokera mu mtima wolungama;
pakamwa panga pakuyankhula zoonadi zimene ndikuzidziwa.
4 Mzimu wa Mulungu wandiwumba,
mpweya wa Wamphamvuzonse umandipatsa moyo.
5 Mundiyankhe ngati mungathe;
konzekani tsopano kuti munditsutse.
6 Ine ndili monga inu pamaso pa Mulungu;
nanenso ndinachokera ku dothi.
7 Musachite mantha ndipo musandiope ayi,
Ine sindikupanikizani kwambiri ayi.

8 “Koma inu mwayankhula ine ndikumva,
ndamva mawu anuwo onena kuti,
9 ‘Ndine wolungama mtima ndi wopanda tchimo;
ndine woyera mtima ndipo ndilibe cholakwa.
10 Komatu Mulungu wapeza zifukwa zoti anditsutsire nazo;
Iye akundiyesa ngati mdani wake.
11 Iyeyo wamanga mapazi anga m’zigologolo,
akulonda mayendedwe anga onse.’

12 “Koma ine ndi kuti kwa inu, inuyo simukukhoza pa zimenezi,
pakuti Mulungu ndi wamkulu kupambana munthu.
13 Chifukwa chiyani mukudandaula kwa Iye
kuti sayankha mawu ena aliwonse a munthu?
14 Pajatu Mulungu amayankhula mwa njira zosiyanasiyana,
ngakhale munthu sazindikira zimenezi.
15 M’maloto, m’masomphenya usiku,

pamene anthu ali m'tulo tofa nato
pamene akungosinza chabe pa bedi,
16 amawanong'oneza m'makutu
ndi kuwaopseza ndi machenjezo ake,
17 kumuchotsa munthu ku zoyipa,
ndi kuthetseratu kunyada kwake,
18 kumulanditsa munthu ku manda,
kuti moyo wake usawonongeke ndi lupanga.

19 "Mwina Mulungu amalanga munthu ndi matenda ndi ululu ali pa bedi pake,
nthawiyo thupi lake lonse limangophwanya,
20 kuti asakhalenso ndi chilakolako cha chakudya,
ndipo amanyansidwa ndi chakudya chabwino chomwe.
21 Thupi lake limawonda
ndipo mafupa ake, omwe anali obisika, tsopano amaonekera poyera.
22 Munthuyo amayandikira ku manda,
moyo wake umayandikira kwa amene amabweretsa imfa.

23 "Koma patakhala mngelo ngati mthandizi,
mmodzi mwa ambirimbiri oterewa,
adzafotokoza zimene zili zoyenera,
24 kudzamukomera mtima ndi kunena kuti,
'Mupulumutseni kuti asapite ku manda;
ine ndapeza cholowa m'malo mwa moyo wake,'
25 pamenepo thupi lake lidzasanduka lasee ngati la mwana;
ndipo adzabwezeretsedwanso kukhala ngati m'masiku a unyamata wake.
26 Akapemphera kwa Mulungu, iyeyo adzalandiridwa.
Mulungu adzamulandira mwa chimwemwe
ndipo adzamubwezeretsa pamalo ake oyamba.
27 Ndipo adzabwera kwa anzake ndi kunena kuti,
'Ndinachimwa ndipo sindinachite zolungama,
koma sindinalangidwe koyenerana ndi kuchimwa kwanga.
28 Iye anapulumutsa moyo wanga kuti usapite ku manda,
ndipo ndidzakhala ndi moyo ndi kuonanso kuwala kwa dzuwa.'

29 "Mulungu amachita zonsezi kwa munthu
kawirikawiri,
30 kupulumutsa moyo wa munthuyo ku manda,
kuti athe kuonanso kuwala kwa moyo.

31 "Abambo Yobu, tcherani khutu ndipo mundimvere;
khalani chete kuti ndiyankhule.
32 Ngati muli n'choti munene, ndiyankheni;
yankhulani, pakuti ine ndikufuna mupezeke wolungama.
33 Koma ngati sichoncho, mundimvere;
khalani chete ndipo ine ndidzakuphunzitsani nzeru."

# 34

1 Pamenepo Elihu anapitiriza kuyankhula kuti,
2 "Imvani mawu anga, inu anthu anzeru;

tcherani khutu inu anthu ophunzira.
3 Pakuti khutu limayesa mawu
monga momwe m'kamwa mumalawira chakudya.
4 Tsono tiyeni tizindikire chomwe chili choyenera;
tiphunzire pamodzi chomwe chili chabwino.

5 "Yobu akunena kuti, 'Ndine wosalakwa,
koma Mulungu akukana kundiweruza molungama.
6 Ngakhale ndine wolungama mtima,
akundiyesa wabodza;
ngakhale ndine wosachimwa,
mivi yake ikundichititsa mabala osachiritsidwa.'
7 Kodi munthu wofanana ndi Yobu ndani,
amene amayankhula zamwano ngati akumwa madzi?
8 Iye amayenda ndi anthu ochita zoyipa;
amayanjana ndi anthu oyipa mtima.
9 Paja iye amanena kuti, 'Munthu sapindula kanthu
poyesetsa kukondweretsa Mulungu.'

10 "Tsono mverani ine, inu anthu anzeru zomvetsa zinthu.
Mulungu sangachite choyipa ndi pang'ono pomwe,
Wamphamvuzonse sangathe kuchita cholakwa.
11 Iye amamubwezera munthu molingana ndi ntchito zake;
Mulungu amabweretsa pa munthu molingana ndi zomwe amachita.
12 N'chosayembekezeka kuti Mulungu achite cholakwa,
kuti Wamphamvuzonse apotoze chilungamo.
13 Kodi anapatsa Mulungu udindo wolamulira dziko lapansi ndani?
Ndani anayika Mulungu kuti azilamulira dziko lonse?
14 Mulungu akanakhala ndi maganizo
oti achotse mzimu wake ndi mpweya wake,
15 zamoyo zonse zikanawonongekeratu
ndipo munthu akanabwerera ku fumbi.

16 "Ngati ndinu omvetsa zinthu, imvani izi;
mvetserani zimene ndikunena.
17 Kodi Mulungu wodana ndi chilungamo angathe kukhala wolamulira?
Kodi iwe ungathe kuweruza Wolungama ndi Wamphamvuyo?
18 Kodi si Iye amene amanena kwa mafumu kuti, 'Ndinu opanda pake,'
ndipo amawuza anthu otchuka, 'Ndinu oyipa,'
19 Iye sakondera akalonga
ndipo salemekeza anthu olemera kupambana osauka,
pakuti onsewa ndi ntchito ya manja ake?
20 Iwo amafa mwadzidzidzi, pakati pa usiku;
anthu amachita mantha ndipo amamwalira;
munthu wamphamvu amachotsedwa popanda dzanja la munthu.

21 "Maso a Mulungu amapenya njira za munthu;
amaona mayendedwe ake onse.
22 Palibe malo obisika kapena a mdima wandiweyani
kumene anthu ochita zoyipa angabisaleko.
23 Mulungu sasowa kuti apitirizebe kufufuza munthu,
kuti abwere pamaso pake kudzaweruzidwa.

24 Popanda kufufuza, Iye amawononga anthu amphamvu
ndipo m'malo mwawo amayikamo ena.
25 Pakuti Iyeyo amadziwa bwino ntchito zawo
amawagubuduza usiku ndipo amatswanyika.
26 Iye amawalanga chifukwa cha kuyipa kwawo,
pamalo pamene aliyense akuwaona;
27 Chifukwa anasiya kumutsata
ndipo sasamaliranso njira zake zonse.
28 Anachititsa amphawi kuti kulira kwawo kufike pamaso pake,
kotero Iyeyo anamva kulira kwa amphawiwo.
29 Koma ngati Mulungu akhala chete, ndani angamunene kuti walakwa?
Akabisa nkhope yake, ndani angathe kumupenyabe?
Komatu ndiye amene amayang'ana za munthu komanso mtundu wa anthu,
30 kuti asalamuliridwe ndi anthu osapembedza,
kuti asatchere anthu misampha.

31 "Mwina munthu atanena kwa Mulungu kuti,
'Ndine wolakwa koma sindidzachimwanso,
32 ndiphunzitseni zimene sindikuziona
ngati ndachita choyipa, sindidzachitanso.'
33 Kodi Mulungu akuweruzeni potsata mmene inuyo mukuganizira,
pamene inu mukukana kulapa?
Chisankho n'chanu, osati changa;
tsono ndiwuzeni zomwe mukudziwa.

34 "Anthu omvetsa zinthu adzakambirana,
anthu anzeru amene akundimva adzandiwuza kuti,
35 'Yobu akuyankhula mopanda nzeru;
mawu ake ndi opanda fundo.'
36 Aa, kunali bwino Yobu akanayesedwa mpaka kumapeto
chifukwa choyankha ngati munthu woyipa!
37 Pa tchimo lake amawonjezerapo kuwukira;
amawomba m'manja mwake monyoza pakati pathu,
ndipo amachulukitsa mawu otsutsana ndi Mulungu."

# 35

1 Ndipo Elihu anawonjeza kunena kuti,
2 "Kodi mukuganiza kuti mukukhoza?
Mukunena kuti, 'Ndine wolungama pamaso pa Mulungu.'
3 Komanso inu mukufunsa kuti, 'Kodi phindu langa n'chiyani,
ndipo ndimapeza chiyani ndikapanda kuchimwa?'

4 "Ine ndikufuna ndikuyankheni inu
pamodzi ndi abwenzi anu omwe.
5 Yang'anani kumwamba ndipo muone
mitambo imene ili kutali ndi inuyo.
6 Inuyo mukachimwa, Iye zimamukhudza motani?
Ngati machimo anu ndi ochuluka, zimenezo zimachita chiyani kwa Iye?
7 Ngati inu ndinu wolungama, mumamupatsa Iyeyo chiyani?
Kapena Iye amalandira chiyani chochokera m'dzanja lanu?

8 Kuyipa kwanu kumangokhudza anthu ngati inuyo,
ndipo chilungamo chanu chimakhudza anthu anzanu.

9 “Anthu akufuwula chifukwa cha kuzunzidwa;
akufuna chithandizo kuti achoke pansi pa ulamuliro wa anthu amphamvu.
10 Koma palibe amene akunena kuti, ‘Kodi ali kuti Mulungu, Mlengi wanga,
amene amatisangalatsa nthawi ya usiku,
11 amene amatiphunzitsa kupambana nyama za dziko lapansi
ndipo amatipatsa nzeru kupambana mbalame zowuluka?’
12 Iye sayankha pamene anthu akufuwulira kwa Iye
chifukwa cha kudzikuza kwa anthu oyipa.
13 Ndithu, Mulungu samva kupempha kwawo kopanda pake;
Wamphamvuzonse sasamalira zimenezi.
14 Ndipo ndi bodza lalikulu kunena kuti
Iye saona zimene zikuchitika.
Iye adzaweruza molungama ngati
inu mutamudikira
15 ndiye tsono popeza kuti ukali wake sukupereka chilango,
zoyipa zambiri zimene anthu amachita,
16 abambo Yobu mumangoyankhula zopandapake,
mukungochulukitsa mawu opanda nzeru.”

# 36

1 Ndipo Elihu anapitirira kuyankhula nati:
2 “Mundilole pang’ono pokha ndipo ndikuonetsani
kuti zilipo zambiri zoti ziyankhulidwe m’malo mwa Mulungu.
3 Nzeru zanga ndimazitenga kutali;
ndidzaonetsa kulungama kwa Mlengi wanga.
4 Ndithudi mawu anga si abodza;
wanzeru zangwiro ali ndi inu.

5 “Mulungu ndi wamphamvu, koma sanyoza anthu;
Iye ndi wamphamvu, ndipo ndi wokhazikika pa cholinga chake.
6 Salola oyipa kuti akhalebe ndi moyo
koma amapereka ufulu kwa anthu osautsidwa.
7 Iye saleka kuyang’anira anthu olungama;
amawayika kuti alamulire pamodzi ndi mafumu
ndipo amawalemekeza mpaka muyaya.
8 Koma ngati anthu amangidwa ndi unyolo,
ndipo akondwa ndi zingwe zamasautso,
9 Iye amawafotokozera zomwe anachita,
kuti iwo anachimwa modzikuza.
10 Mulungu amawatsekula makutu kuti amve malangizo ake
ndipo amawalamula kuti alape zoyipa zawo.
11 Ngati iwo amumvera ndi kumutumikira,
adzatsiriza masiku a moyo wawo mwamtendere,
adzatsiriza zaka zawo mosangalala.
12 Koma ngati samvera,
adzaphedwa ndi lupanga
ndipo adzafa osadziwa kanthu.

13 “Anthu osapembedza amasunga mkwiyo mu mtima mwawo;
akawalanga, safuwulira kwa Iye kupempha thandizo.
14 Amafa akanali achinyamata,
pakati pa amuna achiwerewere a kumalo azipembedzo.
15 Koma ovutika, Iye amawapulumutsa pa mavuto awo;
Mulungu amawayankhula m’masautso awowo.

16 “Iye akukukopani inu kuti muchoke m’masautso,
kuti mupite ku malo aakulu kumene kulibe chokutchingani,
kumalo a mpumulo kumene kuli chakudya chabwino kwambiri.
17 Koma tsopano inu mwapezeka wopalamula chifukwa cha kuyipa kwanu;
chiweruzo ndi chilungamo chakugwerani.
18 Muchenjere kuti wina asakukopeni ndi chuma;
musalole kuti chiphuphu chachikulu chikusocheretseni.
19 Kodi chuma chanu
kapena mphamvu zanu zonse
zingakusungeni kotero kuti simungakhale pa masautso?
20 Musalakalake kuti usiku ubwere,
pakuti ndiyo nthawi imene anthu adzawonongeka.
21 Muchenjere kuti musatembenukire ku uchimo,
chifukwa uchimowo ndiwo unabweretsa kuzunzika kwanu.

22 “Taonani, Mulungu ndi wamkulu ndiponso ndi wamphamvu.
Kodi ndi mphunzitsi uti amene angafanane naye?
23 Kodi ndani amene anamuwuzapo Mulungu zoti achite,
kapena kumuwuza kuti, ‘Inu mwachita chinthu cholakwa?’
24 Kumbukirani kutamanda ntchito zake
zimene anthu amaziyamika m’nyimbo.
25 Anthu onse amaziona ntchitozo;
anthuwo amaziona ali kutali.
26 Ndithudi, Mulungu ndi wamkulu, sitimudziwa n’pang’ono pomwe!
Chiwerengero cha zaka zake n’chosadziwika.

27 “Mulungu ndiye amakweza timadontho tamadzi kuthambo,
timene timasungunuka n’kukhala mvula;
28 mitambo imagwetsa mvulayo
ndipo mvulayo imavumbwa pa anthu mokwanira.
29 Kodi ndani amene angadziwe momwe mitambo imayendera,
momwe Iye amabangulira kuchokera kumalo ake?
30 Taonani momwe amawalitsira zing’aning’ani pa malo ake onse,
zimafika ngakhale pansi pa nyanja.
31 Umu ndi mmene Iye amalamulira mitundu ya anthu
ndi kuwapatsa chakudya chochuluka.
32 Amadzaza manja ake ndi zing’aning’ani,
ndipo amazilamulira kuti zigwe pamalo pamene Iye akufuna.
33 Mabingu ake amalengeza za kubwera kwa mvula yamkuntho;
ng’ombe nazo zimalengeza za kubwera kwake.

# 37

1 “Mtima wanga ukulumphalumpha pa chimenechinso
ndipo ukuchoka m’malo mwake.
2 Tamverani! Tamverani kubangula kwa liwu lake,
kugunda kumene kukuchokera m’kamwa mwake.
3 Iye amaponya ching’aning’ani chake pansi pa thambo lonse
ndipo amachitumiza ku dziko lapansi.
4 Pambuyo pake kubangula kwake kumamveka.
Iye amabangula ndi liwu lake laulemerero.
Pamene wabangula,
palibe chimene amalephera kuchita.
5 Liwu la Mulungu limabangula m’njira zambiri zodabwitsa
Iye amachita zinthu zazikulu zimene sitingathe kuzimvetsa.
6 Amalamula chisanu chowundana kuti, ‘Igwa pa dziko lapansi,’
ndipo amalamulanso mvula yamawawa kuti, ‘Khala mvula yamphamvu.’
7 Kuti anthu onse amene anawalenga athe kuzindikira ntchito yake.
Iye amalepheretsa anthu kugwira ntchito zawo.
8 Zirombo zimakabisala
ndipo zimakhala m’maenje mwawo.
9 Mphepo yamkuntho imatuluka ku malo ake,
kuzizira kumatuluka m’mphepo yamkunthoyo.
10 Mpweya wa Mulungu umawunditsa madzi
ndipo madzi a m’nyanja amawuma kuti gwaa.
11 Iye amadzaza mitambo ndi madzi a mvula,
amabalalitsa zing’aning’ani zake kuchokera m’mitambomo.
12 Mulungu amayendetsa mitamboyo
mozungulirazungulira dziko lonse lapansi
kuti ichite zonse zimene Iye akufuna pa dziko lapansi.
13 Iye amagwetsa mvula kuti alange anthu,
kapena kubweretsa chinyontho pa dziko lapansi kuti aonetse chikondi chake.

14 “Abambo Yobu, tamvani izi;
imani ndipo muganizire ntchito zodabwitsa za Mulungu.
15 Kodi mukudziwa momwe Mulungu amayendetsera mitambo
ndi kuchititsa kuti kukhale zing’aning’ani?
16 Kodi mukudziwa momwe Mulungu amayalira mitambo,
ntchito zodabwitsa za Iye amene ndi wanzeru zangwiro?
17 Inu amene m’zovala zanu mumatuluka thukuta
pamene kunja kwatentha chifukwa cha mphepo yakummwera,
18 kodi mungathe kuthandizana naye kutambasula thambo
limene ndi lolimba ngati chitsulo?

19 “Tiwuzeni ife zoti tikanene kwa Iye;
sitingathe kufotokoza mlandu wathu chifukwa cha mdima umene uli mwa ife.
20 Kodi n’kofunika kumudziwitsa Mulungu kuti ndili naye mawu?
Kodi kutero sikuchita ngati kupempha kuti ndiwonongeke?
21 Tsopano munthu sangathe kuyang’ana dzuwa,
ndi kunyezimira mlengalenga,
kuwomba kwa mphepo kutachotsa mitambo yonse.

22 Kuwala kwake kumaonekera cha kumpoto;
Mulungu amabwera ndi ulemerero woopsa.
23 Wamphamvuzonse sitingathe kumufikira pafupi ndi wa mphamvu zoposa;
pa chiweruzo chake cholungama ndi m'chilungamo chake chachikulu Iye sapondereza anthu ozunzika.
24 N'chifukwa chake anthu amamuopa kwambiri,
kodi saganizira za onse amene amaganiza kuti ndi anzeru?"

# 38

*Yehova Ayankhula*

1 Apo Yehova anamuyankha Yobu m'kamvuluvulu. Ndipo anati:
2 "Kodi uyu ndani amene akusokoneza uphungu wanga
poyankhula mawu opanda nzeru?
3 Onetsa chamuna;
ndikufunsa
ndipo undiyankhe.

4 "Kodi unali kuti pamene ndinkayika maziko a dziko lapansi?
Ndiwuze ngati ukudziwa.
5 Ndani amene analemba malire ake? Ndithudi iwe ukudziwa!
Ndani amene anayeza ndi chingwe dzikoli?
6 Kodi maziko ake anawakumba potani,
kapena ndani anayika mwala wake wapangodya,
7 pamene nyenyezi za kummawa zinkayimba pamodzi
ndipo angelo onse a Mulungu ankafuwula mokondwa?

8 "Kodi ndani amene anatsekera nyanja pamene inkalengedwa,
pamene inkachita ngati kutumphuka pansi pa dziko,
9 pamene ndinasandutsa mitambo kukhala chovala chake
ndi kuyikulunga mu mdima wandiweyani,
10 pamene ndinayilembera malire ake
ndikuyikira zitseko ndi mipiringidzo yake.
11 Pamene ndinati, 'Ufike mpaka apa ndipo usapitirire
apa ndiye pamene mafunde ako amphamvuwo azilekezera?'

12 "Kodi chibadwire chako unalamulapo dzuwa kuti lituluke mmawa,
kapena kuti m'bandakucha ukhalepo pa nthawi yake,
13 kuti kuwalako kuwunikire dziko lonse lapansi
ndi kuthamangitsa anthu oyipa?
14 Chifukwa cha kuwala kwa usana mapiri ndi zigwa zimaonekera bwino ngati zilembo za chidindo pa mtapo;
zimaonekera bwino ngati makwinya a chovala.
15 Kuwala kwa dzuwako sikuwafikira anthu oyipa,
ndipo dzanja lawo silingathe kuchita kanthu.

16 "Kodi unayendapo pansi penipeni pa nyanja
kapena pa magwero ake ozama?
17 Kodi anakuonetsapo zipata za imfa?
Kodi unaonako ku dziko la anthu akufa kumene kuli mdima wandiweyani?

18 Kodi kukula kwa dziko lapansi umakudziwa?
Undiwuze ngati ukuzidziwa zonsezi.

19 “Kodi njira yopita kumene kumakhala kuwala ili kuti?
Nanga mdima umakhala kuti?
20 Kodi iwe ungathe kuziperekeza kwawoko zimenezi?
Kodi ukuyidziwa njira yopita kwawoko?
21 Ndithu, iwe ukuyidziwa, poti paja nthawi imeneyo n’kuti utabadwa kale!
Wakhala ndi moyo zaka zambiridi!

22 “Kodi unalowamo m’nyumba zosungira chisanu chowundana
kapena unayionapo nyumba yosungira matalala,
23 zimene ndazisungira nthawi ya mavuto
ndi nthawi yomenyana ndi ya nkhondo?
24 Kodi umadziwa njira ya kumene kumachokera ching’aning’ani
kapena njira ya kumene kumachokera mphepo ya kummawa imene ili pa dziko lonse lapansi?
25 Kodi ndani amene amakonza ngalande za mvula,
nanga ndani anakonza njira yoyendamo mphenzi,
26 kuthirira madzi dziko limene sikukhala munthu,
chipululu chopandamo munthu,
27 kukhutitsa nthaka yowuma yagwaa
ndi kumeretsamo udzu?
28 Kodi mvula ili ndi abambo ake?
Nanga madzi a mame anawabereka ndani?
29 Kodi madzi owundana anawabereka ndani?
Ndani amene anabereka chisanu chochokera kumwamba
30 pamene madzi amawuma gwaa ngati mwala,
pamene madzi a pa nyanja amazizira, nalimba kuti gwaa?

31 “Kodi iwe ungayimitse kuyenda kwa nyenyezi?
Kodi ungathe kuletsa kuyenda kwa nsangwe ndi akamwiniatsatana?
32 Kodi ungathe kuwongolera nyenyezi pa nyengo yake
kapena kutsogolera nyenyezi yayikulu ya chimbalangondo pamodzi ndi ana ake?
33 Kodi malamulo a mlengalenga umawadziwa?
Kodi ungathe kukhazikitsa ulamuliro wa Mulungu pa dziko lapansi?

34 “Kodi iwe ungathe kulamula mitambo
kuti igwetse mvula ya chigumula?
35 Kodi ungathe kutumiza zing’aning’ani kuti zing’anime?
Kodi zimabwera pamaso pako ndi kuti, ‘Tili pano?’
36 Kodi ndani anayika nzeru mu mtima,
ndani analonga m’maganizo nzeru zomvetsa zinthu?
37 Wanzeru ndani amene angathe kuwerenga mitambo?
Ndani angathe kupendeketsa mitsuko ya madzi akuthambo
38 pamene fumbi limasanduka matope,
ndipo matopewo amawumbika?

39 “Kodi ndani amawusakira chakudya mkango waukazi
ndi kukhutitsa misona ya mikango

40 pamene ili khale m'mapanga mwawo
kapena pamene ikubisala pa tchire?
41 Kodi amamupatsa khwangwala chakudya chake ndani
pamene ana ake akulirira kwa Mulungu
ndi kumayendayenda chifukwa chosowa zakudya?

# 39

1 "Kodi iwe umadziwa nthawi imene mbalale yayikazi imaswera?
Kodi umaonerera pamene nswala ikubala?
2 Kodi umawerenga miyezi imene zimakhala ndi bere?
Kodi nthawi imene zimaswana iwe umayidziwa?
3 Zimakhala tsonga ndi kuswa ana awo;
pamenepo ululu wobereka n'kutha.
4 Ana a nyamazi amakhala ndi mphamvu ndipo amakulira m'thengo;
kenaka amachoka ndipo sabwereranso.

5 "Kodi bulu wakuthengo amamupatsa ndani ufulu wongodziyendera?
Ndani amamasula zingwe zake?
6 Ine ndinamupatsa chipululu kuti chikhale mudzi wake,
nthaka ya mchere kuti ikhale malo ake okhalamo
7 Iye amakhala kutali ndi phokoso la mu mzinda;
ndipo samva kufuwula kwa oyendetsa nyama zakatundu.
8 Amayendayenda m'mapiri kudya msipu
ndipo amafunafuna msipu uliwonse wobiriwira.

9 "Kodi njati ingavomere kukutumikira?
Kodi ingagone mu gome lako usiku?
10 Kodi ungathe kuyimanga ndi zingwe kuti izilima?
Kodi ingasalaze nthumbira m'munda mwako?
11 Kodi ungadalire njatiyo chifukwa champhamvu zake?
Kodi ungayilekere kuti igwire ntchito zako zolemetsa?
12 Kodi ungadalire kuti idzakubweretsera tirigu wako
ndi kumuyika ku malo opunthira?

13 "Nthiwatiwa imakupiza mapiko ake monyadira,
koma mapikowo sangafanane ndi mapiko ndi nthenga za kakowa.
14 Nthiwatiwa imakwirira mazira ake pansi
ndipo amafundidwa ndi nthaka,
15 nthiwatiwayo sidera nkhawa kuti mazira ake angathe kuswanyidwa,
ndi kuti nyama zakuthengo zitha kuwaponda.
16 Nthiwatiwa imachitira nkhanza ana ake ngati anawo si ake;
Imayiwala zoti inavutika powabala.
17 Chifukwa Mulungu anayimana nzeru,
simvetsa kanthu kalikonse.
18 Komatu nthiwatiwa ikadzambatuka ndi kuyamba kuthamanga,
imamusiya kutali kavalo ndi wokwerapo wake.

19 "Kodi ndiwe amene umamupatsa mphamvu kavalo
kapena kumuveka chenjerere m'khosi mwake?
20 Kodi ndiwe amene umalipatsa dzombe ulemerero wolumphira,

ukali wake n'kumachititsa mantha?
21 Iye amalumphalumpha moopseza, kukondwerera mphamvu zake,
ndipo amapita ku nkhondo ndi mphamvu zake zonse.
22 Iye sachita mantha, saopa chilichonse;
sabwerera m'mbuyo akaona lupanga.
23 Zida zankhondo zimachita kwichikwichi m'chimake pambali pake
pamodzi ndi mkondo wonyezimira ndi nthungo.
24 Kavaloyo amanjenjemera ndi ukali ndi kulumphalumpha;
satha kungoyima pamene wamva kulira kwa lipenga.
25 Lipenga likalira amati, 'Twee!'
Amamva fungo la nkhondo ali patali,
kufuwula kwa anthu olamulira nkhondo ndi mfuwu wankhondo.

26 "Kodi kabawi amawuluka ndi nzeru zako,
ndi kutambasula mapiko ake kupita kummwera?
27 Kodi umalamulira chiwombankhanga ndiwe kuti chiziwuluka
ndi kumanga chisa chake pamwamba penipeni?
28 Chimakhala pa phiri ndipo chimakhala pamenepo usiku;
chimakhala pa msonga penipeni pa mwala.
29 Chili pamenepo chimayang'anayang'ana choti chigwire kuti chidye;
maso ake amachionera patali chinthucho.
30 Ana ake amayamwa magazi,
ndipo kumene kuli mitembo ndiko chimapezeka."

# 40

1 Yehova anati kwa Yobu:
2 "Kodi iwe ufuna kukangana ndi Wamphamvuzonse?
Iwe amene unatsutsana ndi Mulungu umuyankhe Iyeyo!"
3 Pamenepo Yobu anayankha Yehova:
4 "Ine sindili kanthu konse,
kodi ndingathe kukuyankhani chiyani? Ndagwira pakamwa panga.
5 Ndinayankhula kamodzi, koma pano ndilibe yankho,
ndinayankha kawiri, koma sindiwonjezeranso mawu ena."
6 Ndipo Yehova anayankha Yobu m'kamvuluvulu kuti,
7 "Tsopano vala dzilimbe ngati mwamuna;
ndikufunsa mafunso
ndipo iwe undiyankhe.

8 "Kodi iwe unganyoze chiweruzo changa cholungama?
Kodi ungandidzudzule kuti iweyo ukhale wolungama?
9 Kodi uli ndi dzanja monga la Mulungu,
ndipo mawu ako angagunde ngati mphenzi monga a Mulungu?
10 Ngati zili choncho udzikometsere ndi ulemerero ndi kukongola,
ndipo udziveke ulemu ndi ulemerero waufumu.
11 Tsanula ukali wako wosefukirawo,
uyang'ane aliyense wodzikuza ndipo umuchepetse,
12 Uyang'ane aliyense wodzikweza ndipo umutsitse,
uwapondereze oyipa onse pamalo pomwe alilipo.
13 Onsewo uwakwirire pamodzi mfumbi;
ukulunge nkhope zawo m'manda.
14 Ukatero Ine ndidzakuvomereza

kuti dzanja lako lamanja lakupulumutsadi.

15 “Taganiza za mvuwu,
imene ndinayipanga monga momwe ndinapangira iwe,
ndipo imadya udzu ngati ng’ombe.
16 Mphamvu zake ndi zazikulu kwambiri,
thupi lake ndi lanyonga kwambiri!
17 Mchira wake umayima tolotolo ngati mtengo wamkungudza;
mitsempha ya ntchafu zake ndi yogwirana bwino.
18 Mafupa ake ali ngati mapayipi amkuwa,
nthiti zake zili ngati mipiringidzo yachitsulo.
19 Mvuwuyo ndi yayikulu mwa zolengedwa za Mulungu,
komatu mlengi wake amatha kuyiopseza ndi lupanga lake.
20 Imapeza chakudya chake ku mtunda
ndipo nyama zakuthengo zonse zimasewera pambali pake.
21 Imagona pa tsinde pa zitsamba za mipeta,
imabisala m’bango ndiponso pa thawale.
22 Imaphimbika ndi mthunzi wazitsamba za mipeta;
imazunguliridwa ndi misondozi ya mu mtsinje.
23 Madzi a mu mtsinje akakokoma, sichita mantha,
iyo sitekeseka, ngakhale madzi a mu Yorodani afike m’khosi mwake.
24 Kodi alipo amene angathe kukola mvuwu ndi mbedza
kapena kuyikola mu msampha?

# 41

1 “Kodi ungathe kukoka ng’ona ndi mbedza ya nsomba
kapena kukanikiza lilime lake pansi ndi chingwe?
2 Kodi ungathe kumanga chingwe m’mphuno mwake,
kapena kubowola nsagwada zake ndi mbedza?
3 Kodi ng’onayo idzakupempha kuti uyichitire chifundo?
Kodi idzakuyankhula ndi mawu ofatsa?
4 Kodi idzachita nawe mgwirizano
kuti uyisandutse kapolo wako mpaka muyaya?
5 Kodi udzasewera nayo ngati mbalame,
kapena kuyimangirira kuti atsikana ako asewere nayo?
6 Kodi anthu adzayitsatsa malonda?
Nanga amalondawo n’kugawanagawana nyama yake kuti akagulitse?
7 Kodi chikopa chake ungathe kuchilasa ndi zisonga,
kapena kubowola mutu wake ndi nthungo zophera nsomba?
8 Ukayiputa udziwe kuti pali nkhondo,
ndipo iweyo sudzabwereranso.
9 Chiyembekezo choti n’kuyigonjetsa ndi chabodza;
kungoyiona kokha, ndithu iwe kumangodzigwera wekha.
10 Palibe wolimba mtima kuti ndi kuyiputa.
Ndani angalimbe mtima kulimbana ndi Ine?
11 Kodi ndani anandipatsa kanthu kuti ndimubwezere?
Zonse za pansi pa thambo ndi zanga.

12 “Sindidzaleka kuyankhula za ziwalo zake za chirombocho,
za mphamvu zake ndiponso za maonekedwe a thupi lake.

13 Ndani angasende chikopa chake?
Ndani angayiyandikire kuti abowole chikopa chake cholimbacho?
14 Ndani angatsekule kukamwa kwake,
pakamwa pamene pazunguliridwa ndi mano ochititsa mantha?
15 Kumsana kwake kuli mizere ya mamba
onga zishango zolumikizanalumikizana;
16 Mambawo ndi olukanalukana
kotero kuti mpweya sungathe kulowa pakati pake.
17 Ndi olumikizanalumikizana;
ndi omatirirana kwambiri kotero kuti sangathe kulekana.
18 Kuyetsemula kwake kumatulutsa mbaliwali;
maso ake amawala ngati kuwala kwa m'bandakucha.
19 M'kamwa mwake mumatuluka nsakali zamoto ndipo
mumathetheka mbaliwali zamoto.
20 M'mphuno mwake mumatuluka utsi
ngati wa m'nkhali yowira yomwe ili pa moto wa bango.
21 Mpweya wake umayatsa makala,
ndipo malawi amoto amatuluka m'kamwa mwake.
22 Mphamvu zake zili m'khosi mwake;
aliyense wokumana nayo amangoti njenjenje ndi mantha.
23 Minyewa ya thupi lake ndi yolumikizana ndipo
ndi yokhwima kwambiri ndi yolimba.
24 Pachifuwa pake ndi powuma ngati mwala,
ndi pa gwaa, ngati mwala wamphero.
25 Ng'onayo ikangovuwuka,
ndi anthu amphamvu omwe amaopa; amabwerera m'mbuyo,
kuthawa.
26 Ngakhale ikanthidwe ndi lupanga, lupangalo silichita kanthu,
ngakhale mkondo, muvi ndi nthungo, zonse zimalephera.
27 Chitsulo imachiyesa ngati phesi chabe
ndi mkuwa ngati chikuni chowola.
28 Muvi sungathe kuyithawitsa,
miyala imene ayilasa nayo imangoyinyenyanyenya.
29 Zibonga zimakhala ngati ziputu;
imangoseka pamene akuyibaya ndi nthungo.
30 Mamba a ku mimba kwake ali ngati chopunthira chakunthwa ndipo
imasiya mkukuluzi m'matope ngati galeta lopunthira tirigu.
31 Imagadutsa madzi ozama ngati madzi a m'nkhali,
imachititsa nyanja kuti iwire ngati mbiya yoyengera mafuta.
32 Kumbuyo kwake imasiya nthubwitubwi zambee,
kotero kuti munthu angaganize kuti nyanja yachita imvi.
33 Pa dziko lapansi palibe china chofanana nacho,
n'cholengedwa chopanda mantha.
34 Chimanyoza nyama zina zonse;
icho chija ndi mfumu ya nyama zonse."

# 42

*Yobu*

1 Pamenepo Yobu anayankha Yehova kuti,
2 "Ndikudziwa kuti Inu mungathe kuchita zinthu zonse;
chimene mufuna kuchita wina sangaletse konse.

3 Munandifunsa kuti, ‘Kodi ndiwe yani amene ukufuna kusokoneza
uphungu wanga ndi mawu opanda nzeru?
Zoonadi ndinayankhula zimene sindinazimvetse,
zinthu zodabwitsa kwambiri kwa ine zimene sindinazidziwe.

4 “Inu munandiwuza kuti, ‘Mvetsetsa tsopano ndipo ndidzayankhula;
ndidzakufunsa
ndipo iwe udzandiyankhe.’
5 Ndinkangomva za Inu ndi makutu anga,
koma tsopanonso ndakuonani ndi maso anga.
6 N’chifukwa chake ndi kuchita manyazi,
ndikulapa podzithira fumbi ndi phulusa.”

*Mulungu Adalitsa Yobu*

7 Yehova atayankhula ndi Yobu mawu amenewa anawuza Elifazi wa
ku Temani kuti, “Ine ndakukwiyira pamodzi ndi abwenzi ako awiri,
chifukwa simunayankhule zabwino za Ine, monga mmene wayankhulira
mtumiki wanga Yobu. 8 Kotero tsopano mutenge ng’ombe zazimuna
zisanu ndi ziwiri ndi nkhosa zazimuna zisanu ndi ziwiri ndi kupita nazo
kwa mtumiki wanga Yobu kuti mukapereke nsembe zopsereza. Mtumiki
wanga Yobu adzakupemphererani, ndipo Ine ndidzalandira pemphero
lake. Sindidzakuchitirani kanthu molingana ndi uchitsiru wanu. Inu
simunayankhule zabwino za Ine, monga anayankhulira Yobu mtumiki
wanga.” 9 Motero Elifazi wa ku Temani, Bilidadi wa ku Suki ndi Zofari wa
ku Naama anachita zimene Yehova anawawuza ndipo Yehova anamvera
pemphero la Yobu.

10 Yobu atawapempherera abwenzi ake aja, Yehova anamubwezera
chuma chake ndipo anamupatsa mowirikiza kuposa zomwe anali nazo
kale. 11 Abale ake ndi alongo ake onse, kuphatikizapo onse amene
ankamudziwa kale, amabwera kwa iye n’kudzadya naye chakudya
m’nyumba mwake. Iwo anamutonthoza ndi kumupepesa chifukwa cha
mavuto onse amene Yehova analola kuti amugwere. Aliyense wa iwowa
anamupatsa ndalama ndi mphete yagolide.

12 Yehova anadalitsa Yobu pa masiku ake otsirizawa kupambana
poyamba paja. Iye anali ndi nkhosa 14,000, ngamira 6,000, ng’ombe
zantchito 2,000 ndi abulu aakazi 1,000. 13 Anaberekanso ana aamuna
asanu ndi awiri ndi ana aakazi atatu. 14 Mwana wake wamkazi woyamba
anamutcha Yemima, wachiwiri anamutcha Keziya, wachitatu anamutcha
Kereni Hapuki. 15 M’dziko monsemo munalibe akazi okongola ngati ana a
Yobu, ndipo abambo awo anawapatsa cholowa pamodzi ndi alongo awo.

16 Zitachitika zimenezi, Yobu anakhala ndi moyo zaka 140. Iye anaona
zidzukulu zake mpaka m’bado wachinayi. 17 Potsiriza, Yobu anamwalira
ali nkhalamba ya zaka zochuluka kwambiri.

# Masalimo
## BUKU LOYAMBA
# 1

*Masalimo 1–41*
1 Wodala munthu
amene satsatira uphungu wa anthu ochimwa,
kapena kuyima m'njira ya anthu oyipa,
kapena kukhala m'magulu a anthu onyoza.
2 Koma chikondwerero chake chili m'malamulo a Yehova
ndipo m'malamulo akewo amalingaliramo usana ndi usiku.
3 Iye ali ngati mtengo wodzalidwa m'mbali mwa mitsinje ya madzi,
umene umabereka zipatso zake pa nyengo yake
ndipo masamba ake safota.
Chilichonse chimene amachita amapindula nacho.
4 Sizitero ndi anthu oyipa!
Iwo ali ngati mungu
umene umawuluzidwa ndi mphepo.
5 Kotero anthu oyipa sadzatha kuyima pa chiweruzo,
kapena anthu ochimwa mu msonkhano wa anthu olungama.

6 Pakuti Yehova amayang'anira mayendedwe a anthu olungama,
koma mayendedwe a anthu oyipa adzawonongeka.

# Salimo 2

1 N'chifukwa chiyani anthu a mitundu ina akufuna kuchita chiwembu?
Akonzekeranji zopanda pake anthu?
2 Mafumu a dziko lapansi akugwirizana nazo;
ndipo olamulira asonkhana pamodzi
kulimbana ndi Ambuye
ndi wodzozedwa wakeyo.
3 Iwo akunena kuti, "Tiyeni timasule magoli awo
ndipo titaye zingwe zawo."

4 Wokhala mmwamba akuseka;
Ambuye akuwanyoza iwowo.
5 Ndipo iye awadzudzula mu mkwiyo wake
ndi kuwaopseza mu ukali wake, kunena kuti,
6 "Ine ndakhazikitsa mfumu yanga
pa Ziyoni, phiri langa loyera."
7 Ine ndidzalengeza zimene Yehova walamula:
Iye anati kwa Ine, "Iwe ndiwe mwana wanga;
lero Ine ndakhala Atate ako.
8 Tandipempha,
ndipo ndidzachititsa kuti mitundu ya anthu ikhale cholowa chako;
malekezero a dziko lapansi kuti akhale chuma chako.
9 Iweyo udzawalamulira ndi ndodo yaufumu yachitsulo;
udzawaphwanya zidutswazidutswa ngati zowumba zadothi."

10 Kotero, inu mafumu, chenjerani;

chenjezedwani, inu olamulira a dziko lapansi.
11 Tumikirani Yehova mwa mantha
ndi kukondwerera ulamuliro wake monjenjemera.
12 Mpsopsoneni mwanayo kuti angakwiye;
kuti mungawonongedwe m'njira zanu,
pakuti ukali wake utha kuuka m'kanthawi kochepa.
Odala ndi onse amene amathawira kwa Iye.

# Salimo 3

Salimo la Davide. Atathawa mwana wake Abisalomu.
1 Inu Yehova, achulukadi adani anga!
Achulukadi amene andiwukira!
2 Ambiri akunena za ine kuti,
"Mulungu sadzamupulumutsa."

Sela

3 Koma Inu Yehova, ndinu chishango chonditeteza,
Inu mwandiveka ulemerero ndipo mwanditukula.
4 Kwa Yehova, Ine ndilira mofuwula
ndipo Iye amandiyankha kuchokera ku phiri lake loyera.

Sela

5 Ine ndimagona ndi kupeza tulo;
ndimadzukanso chifukwa Yehova amandichirikiza.
6 Sindidzaopa adani anga osawerengeka amene
abwera kulimbana nane kuchokera ku madera onse.

7 Dzukani, Inu Yehova!
Pulumutseni, Inu Mulungu wanga.
Akantheni adani anga onse pa msagwada;
gululani mano a anthu oyipa.

8 Chipulumutso chimachokera kwa Yehova.
Madalitso akhale pa anthu anu.

Sela

# Salimo 4

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe wa zida za zingwe. Salimo la Davide.
1 Ndiyankheni pamene ndiyitana Inu,
Inu Mulungu wa chilungamo changa.
Pumulitseni ku zowawa zanga;
chitireni chifundo ndi kumva pemphero langa.

2 Anthu inu, mpaka liti mudzakhala mukusandutsa ulemerero wanga kukhala manyazi?
Mpaka liti mudzakonda zachabe ndi kufuna milungu yabodza?
Sela.
3 Dziwani kuti Yehova wadziyikira padera anthu okhulupirika;
Yehova adzamva pamene ndidzamuyitana.

4 Kwiyani koma musachimwe;
pamene muli pa mabedi anu,
santhulani mitima yanu ndi kukhala chete.

Sela

5 Perekani nsembe zolungama
ndipo dalirani Yehova.

6 Ambiri akufunsa kuti, “Ndani angationetse chabwino chilichonse?”
Kuwunika kwa nkhope yanu kutiwalire, Inu Yehova.
7 Inu mwadzaza mtima wanga ndi chimwemwe chachikulu
kuposa kuchuluka kwa tirigu wawo ndi vinyo watsopano.
8 Ine ndidzagona ndi kupeza tulo mwamtendere,
pakuti Inu nokha, Inu Yehova,
mumandisamalira bwino.

# Salimo 5

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe zoyimbira za zitoliro. Salimo la Davide.

1 Tcherani khutu ku mawu anga, Inu Yehova,
ganizirani za kusisima kwanga
2 Mverani kulira kwanga kofuna thandizo,
Mfumu yanga ndi Mulungu wanga,
pakuti kwa Inu, ine ndikupemphera.
3 Mmawa, Yehova mumamva mawu anga;
Mmawa ndimayala zopempha zanga pamaso panu
ndi kudikira mwachiyembekezo.

4 Inu si Mulungu amene mumasangalala ndi zoyipa;
choyipa sichikhala pamaso panu.
5 Onyada sangathe kuyima pamaso panu;
Inu mumadana ndi onse ochita zoyipa.
6 Mumawononga iwo amene amanena mabodza;
anthu akupha ndi achinyengo,
Yehova amanyansidwa nawo.

7 Koma Ine, mwa chifundo chanu chachikulu,
ndidzalowa m’Nyumba yanu;
mwa ulemu ndidzaweramira pansi
kuyang’ana ku Nyumba yanu yoyera.
8 Tsogolereni Inu Yehova, mwa chilungamo chanu
chifukwa cha adani anga ndipo
wongolani njira yanu pamaso panga.

9 Palibe mawu ochokera m’kamwa mwawo amene angadalirike;
mtima wawo wadzaza ndi chiwonongeko.
Kummero kwawo kuli ngati manda apululu;
ndi lilime lawo amayankhula zachinyengo.
10 Lengezani kuti ndi olakwa, Inu Mulungu!
Zochita zawo zoyipa zikhale kugwa kwawo.
Achotseni pamaso panu chifukwa cha machimo awo ambiri,
pakuti awukira Inu.

11 Koma lolani kuti onse amene apeza chitetezo mwa Inu akondwere;
lolani kuti aziyimba nthawi zonse chifukwa cha chimwemwe.
Aphimbeni ndi chitetezo chanu,
iwo amene amakonda dzina lanu akondwere mwa Inu.

12 Ndithu, Inu Yehova, mumadalitsa olungama;
mumawazungulira ndi kukoma mtima kwanu ngati chishango.

# Salimo 6

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Pa zoyimbira za zingwe. Molingana ndi seminiti. Salimo la Davide.

1 Inu Yehova, musandidzudzule mu mkwiyo wanu,
kapena kundilanga mu ukali wanu.
2 Ndichitireni chifundo Inu Yehova, pakuti ndalefuka;
Inu Yehova chiritseni, pakuti mafupa anga ali pa ululu waukulu.
3 Moyo wanga uli pa mazunzo aakulu.
Mpaka liti, Inu Yehova, mpaka liti?

4 Tembenukani Inu Yehova, ndipo mundilanditse;
pulumutseni chifukwa cha chikondi chanu chosasinthika.
5 Palibe amene amakukumbukirani pamene wamwalira;
Amakutamandani ndani ali ku manda?

6 Ine ndatopa ndi kubuwula;
usiku wonse pa bedi panga pamadzaza ndi misozi yanga;
ndimanyowetsa pogona panga ndi misozi.
7 Maso anga atupa chifukwa cha chisoni;
akulephera kuona chifukwa cha adani anga.

8 Chokani kwa ine inu nonse amene mumachita zoyipa,
pakuti Yehova wamva kulira kwanga.
9 Yehova wamva kupempha kwanga kofuna chifundo;
Yehova walandira pemphero langa.
10 Adani anga onse adzachita manyazi ndipo adzakhala ndi mantha;
adzabwerera msangamsanga mwa manyazi.

# Salimo 7

Sigioni wa Davide, amene anayimbira Yehova zokhudza Kusi, wa fuko la Benjamini.

1 Inu Yehova Mulungu wanga, Ine ndikuthawira kwa Inu;
pulumutseni ndi kundilanditsa kwa onse amene akundithamangitsa,
2 mwina angandikadzule ngati mkango,
ndi kunding'amba popanda wondipulumutsa.

3 Inu Yehova Mulungu wanga,
ngati ndachita izi ndipo ndapezeka wolakwa,
4 ngati ndachita zoyipa kwa iye amene ndili naye pa mtendere,
kapena popanda chifukwa ndalanda mdani wanga,
5 pamenepo lolani adani anga andithamangitse ndi kundipitirira,
lolani kuti moyo wanga aupondereze pansi
ndipo mundigoneke pa fumbi.

Sela

6 Nyamukani Yehova, mu mkwiyo wanu;
nyamukani kutsutsana ndi mkwiyo wa adani anga.
Dzukani Mulungu wanga, lamulirani chilungamo chanu.

7 Lolani gulu la anthu a mitundu ina lisonkhane mokuzungulirani.
Alamulireni muli kumwambako;
8 Yehova aweruzeni anthu a mitundu inayo.
Ndiweruzeni Yehova, monga mwa chilungamo changa,
monga mwa moyo wanga wangwiro, Inu Wammwambamwamba.
9 Inu Mulungu wolungama,
amene mumasanthula maganizo ndi mitima,
thetsani chiwawa cha anthu oyipa
ndipo wolungama akhale motetezedwa.

10 Chishango changa ndi Mulungu Wammwambamwamba,
amene amapulumutsa olungama mtima.
11 Mulungu amaweruza molungama,
Mulungu amene amaonetsa ukali wake tsiku ndi tsiku.
12 Ngati munthu satembenuka,
Mulungu adzanola lupanga lake,
Iye adzawerama ndi kukoka uta.
13 Mulungu wakonza zida zake zoopsa;
Iye wakonzekera mivi yake yoyaka moto.

14 Taonani, munthu woyipa amalingalira zoyipa zokhazokha nthawi zonse.
Zochita zake ndi zosokoneza ndi zovutitsa anthu ena.
15 Iye amene akumba dzenje ndi kulizamitsa
amagwera m'dzenje limene wakumbalo.
16 Mavuto amene amayambitsa amamubwerera mwini;
chiwawa chake chimatsikira pa mutu wake womwe.

17 Ine ndidzayamika Yehova chifukwa cha chilungamo chake;
ndipo ndidzayimba nyimbo zamatamando pa dzina la Yehova Wammwambamwamba.

# Salimo 8

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Pa gititi. Salimo la Davide.
1 Inu Yehova Ambuye athu,
dzina lanu ndi la lamphamvudi pa dziko lonse lapansi!

Inu mwakhazikitsa ulemerero wanu
m'mayiko onse akumwamba.
2 Kuchokera m'kamwa mwa ana ndi makanda,
Inu mwakhazikitsa mphamvu
chifukwa cha adani anu,
kukhazikitsa bata adani ndi anthu obwezera zoyipa.

3 Pamene ndilingalira za mayiko anu akumwamba,
ntchito ya zala zanu,
mwezi ndi nyenyezi,
zimene mwaziyika pa malo ake,
4 munthu ndani kuti Inu mumamukumbukira,
ndi mwana wa munthu kuti inu mumacheza naye?
5 Inu munamupanga kukhala wocheperapo kusiyana ndi zolengedwa zakumwamba
ndipo mwamuveka ulemerero ndi ulemu.

6 Inu munamuyika wolamulira ntchito ya manja anu;
munayika zinthu zonse pansi pa mapazi ake;
7 nkhosa, mbuzi ndi ng'ombe pamodzi
ndi nyama zakuthengo,
8 mbalame zamlengalenga
ndi nsomba zam'nyanja
zonse zimene zimayenda pansi pa nyanja.

9 Inu Yehova, Ambuye athu,
dzina lanu ndi lamphamvudi pa dziko lonse lapansi!

# Salimo 9

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Monga mwa mayimbidwe a nyimbo ya “Imfa ya Mwana.” Salimo la Davide.

1 Ine ndidzakutamandani, Inu Yehova, ndi mtima wanga wonse;
ndidzafotokoza za zodabwitsa zanu zonse.
2 Ndidzakondwa ndi kusangalala mwa inu;
Ndidzayimba nyimbo zamatamando pa dzina lanu, Inu Wammwambamwamba.

3 Adani anga amathawa,
iwo amapunthwa ndi kuwonongedwa pamaso panu.
4 Pakuti Inu mwatsimikiza za kulungama kwanga ndi mlandu wanga;
Inu mwakhala pa mpando wanu waufumu, kuweruza mwachilungamo.
5 Mwadzudzula mitundu ya anthu ndipo mwawononga anthu oyipa;
Inu mwafafaniza dzina lawo kwamuyaya.
6 Chiwonongeko chosatha chagwera adani,
mwafafaniza mizinda yawo;
ngakhale chikumbutso chawo chawonongedwa.

7 Yehova akulamulira kwamuyaya;
wakhazikitsa mpando wake waufumu woweruzira.
8 Iye adzaweruza dziko mwachilungamo;
adzalamulira mitundu ya anthu mosakondera.
9 Yehova ndiye kothawirako kwa opsinjika mtima,
linga pa nthawi ya mavuto.
10 Iwo amene amadziwa dzina lanu adzadalira Inu,
pakuti Inu Yehova, simunawatayepo amene amafunafuna inu.

11 Imbani nyimbo zamatamando kwa Yehova, ali pa mpando waufumu mu Ziyoni;
lengezani pakati pa mitundu ya anthu zimene wachita.
12 Pakuti Iye amene amabwezera chilango akupha anzawo wakumbukira;
Iye salekerera kulira kwa ozunzika.

13 Inu Yehova, onani momwe adani anga akundizunzira!
Chitireni chifundo ndipo ndichotseni pa zipata za imfa,
14 kuti ndilengeze za matamando anu
pa zipata za ana aakazi a Ziyoni,
kuti pamenepo ndikondwere ndi chipulumutso chanu.

15 Mitundu ya anthu yagwa m'dzenje limene yakumba;
mapazi awo akodwa mu ukonde umene anawubisa.
16 Yehova amadziwika ndi chilungamo chake;
oyipa akodwa ndi ntchito za manja awo.
Higayoni. Sela
17 Oyipa amabwerera ku manda,
mitundu yonse imene imayiwala Mulungu.
18 Koma osowa sadzayiwalika nthawi zonse,
kapena chiyembekezo cha ozunzika kutayika nthawi zonse.

19 Dzukani Inu Yehova, musalole munthu kuti apambane;
mitundu yonse iweruzidwe pamaso panu.
20 Akantheni ndi mantha aakulu, Inu Yehova;
mitundu idziwe kuti iwo ndi anthu wamba.
Sela

# Salimo 10

1 N'chifukwa chiyani Yehova mwayima patali?
Chifukwa chiyani mukudzibisa nokha pa nthawi ya mavuto?

2 Mwa kunyada kwake munthu woyipa asaka wofowoka,
amene akodwa m'njira zimene iye wakonza.
3 Iye amatamandira zokhumba za mu mtima wake;
amadalitsa aumbombo ndi kuchitira chipongwe Yehova.
4 Mwa kunyada kwake woyipa safunafuna Mulungu;
m'maganizo ake wonse mulibe malo a Mulungu.
5 Zinthu zake zimamuyendera bwino;
iye ndi wamwano ndipo malamulo anu ali nawo kutali;
amanyogodola adani ake onse.
6 Iye amadziyankhulira kuti, "Palibe chimene chidzandigwedeze.
Ndidzakhala wokondwa nthawi zonse ndipo sindidzakhala pa mavuto."
7 M'kamwa mwake mwadzaza matemberero, mabodza ndi zoopseza;
zovutitsa ndi zoyipa zili pansi pa lilime lake.
8 Iye amabisalira anthu pafupi ndi midzi,
kuchokera pobisalapo amapha anthu osalakwa,
amayang'anayang'ana mwachinsinsi anthu oti awawononge.
9 Amabisalira anthu ngati mkango pa zitsamba.
Amabisalira kuti agwire anthu opanda mphamvu;
amagwira anthu opanda mphamvu ndi kuwakokera mu ukonde wake.
10 Anthuwo amawapondaponda ndipo amakomoka;
amakhala pansi pa mphamvu zake.
11 Iye amati mu mtima mwake, "Mulungu wayiwala,
wabisa nkhope yake ndipo sakuonanso."

12 Dzukani Yehova! Onetsani dzanja lanu Inu Mulungu.
Musayiwale anthu opanda mphamvu.
13 N'chifukwa chiyani munthu woyipa amachitira chipongwe Mulungu?
Chifukwa chiyani amati mu mtima mwake,
"Iye sandiyimba mlandu?"
14 Komatu Inu Mulungu, mumazindikira mavuto ndi zosautsa,
mumaganizira zochitapo kanthu.

Wovutikayo amadzipereka yekha kwa Inu pakuti
Inu ndi mthandizi wa ana amasiye.
15 Thyolani dzanja la woyipitsitsa ndi la munthu woyipa;
muzengeni mlandu chifukwa cha zoyipa zake
zimene sizikanadziwika.

16 Yehova ndi Mfumu kwamuyaya;
mitundu ya anthu idzawonongeka kuchoka m'dziko lake.
17 Mumamva Inu Yehova, zokhumba za osautsidwa;
mumawalimbikitsa ndipo mumamva kulira kwawo.
18 Kuteteza ana amasiye ndi oponderezedwa,
ndi cholinga chakuti munthu amene ali wa dziko lapansi asaopsenso.

# Salimo 11

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Mwa Yehova ine ndimathawiramo.
Nanga mungathe bwanji kunena kwa ine kuti,
"Thawira ku phiri lako ngati mbalame.
2 Pakuti taona oyipa akunga mauta awo;
ayika bwino mivi yawo pa zingwe za uta,
pobisala pawo kuti alase
olungama mtima.
3 Tsono ngati maziko awonongeka,
olungama angachite chiyani?"

4 Yehova ali m'Nyumba yake yoyera;
Yehova ali pa mpando wake waufumu kumwamba.
Iye amayang'anitsitsa ana a anthu;
maso ake amawayesa.
5 Yehova amayesa olungama,
koma moyo wake umadana ndi oyipa,
amene amakonda zachiwawa.
6 Iye adzakhuthulira pa oyipa
makala amoto ndi sulufule woyaka;
mphepo yotentha idzakhala yowayenera.

7 Pakuti Yehova ndi wolungama,
Iye amakonda chilungamo;
ndipo anthu olungama adzaona nkhope yake.

# Salimo 12

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Monga mwa mayimbidwe seminiti. Salimo la Davide.
1 Thandizeni Yehova pakuti palibe munthu wokhulupirika;
okhulupirika akusowa pakati pa anthu.
2 Aliyense amanamiza m'bale wake;
ndi pakamwa pawo pabodza amayankhula zachinyengo.

3 Inu Yehova tsekani milomo yonse yachinyengo
ndi pakamwa paliponse podzikuza.
4 Pakamwa pamene pamati, "Ife tidzapambana ndi kuyankhula kwathu;
pakamwapa ndi pathupathu, tsono mbuye wathu ndani?"

5 “Chifukwa cha kuponderezedwa kwa anthu opanda mphamvu
ndi kubuwula kwa anthu osowa,
Ine ndidzauka tsopano,” akutero Yehova,
“Ndidzawateteza kwa owazunza.”
6 Ndipo mawu a Yehova ndi angwiro
monga siliva oyengedwa m’ng’anjo yadothi,
oyengedwa kasanu n’kawiri.

7 Inu Yehova mudzatitchinjiriza ndipo
mudzatiteteza kwa anthu otere kwamuyaya.
8 Oyipa amangoyendayenda ponseponse
anthu akamayamikira zochita zawo.

# Salimo 13

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Mpaka liti Yehova? Kodi mudzandiyiwala mpaka kalekale?
Mpaka liti mudzandibisira nkhope yanu?
2 Ndidzalimbana ndi maganizo anga
ndi kukhala ndi chisoni mu mtima mwanga tsiku lililonse mpaka liti?
Mpaka liti adani anga adzandipambana?

3 Ndiyang’aneni ndi kundiyankha, Inu Yehova Mulungu wanga.
Walitsani maso anga kuti ndingafe;
4 mdani wanga adzati, “Ndamugonjetsa,”
ndipo adani anga adzakondwera pamene ine ndagwa.

5 Koma ndikudalira chikondi chanu chosasinthika;
mtima wanga umakondwera ndi chipulumutso chanu.
6 Ine ndidzayimbira Yehova
pakuti wandichitira zokoma.

# Salimo 14

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Chitsiru chimati mu mtima mwake,
“Kulibe Mulungu.”
Oterewa ndi oyipa ndipo ntchito zawo ndi zonyansa;
palibe amene amachita zabwino.

2 Yehova kumwamba wayang’ana pansi,
kuyang’ana anthu onse
kuti aone ngati alipo wina wanzeru,
amene amafunafuna Mulungu.
3 Onse atembenukira kumbali,
onse pamodzi asanduka oyipa;
palibe amene amachita zabwino,
palibiretu ndi mmodzi yemwe.

4 Kodi anthu ochita zoyipawa sadziwa chilichonse?
Akudya anthu anga ngati chakudya chawo
ndipo satamanda Yehova?
5 Awo ali apowo, agwidwa ndi mantha aakulu,
pakuti Mulungu ali m’gulu la olungama.

6 Inu ochita zoyipa mumalepheretsa chikonzero cha anthu osauka,
koma Yehova ndiye pothawirapo pawo.

7 Ndithu, chipulumutso cha Israeli chidzachokera ku Ziyoni!
Pamene Yehova abwezeretsa ufulu wa anthu ake,
Yakobo akondwere ndipo Israeli asangalale!

# Salimo 15

Salimo la Davide.
1 Yehova, ndani angathe kukhala m'malo anu opatulika?
Kodi ndani angathe kukhala m'phiri lanu loyera?

2 Munthu wa makhalidwe abwino,
amene amachita zolungama,
woyankhula choonadi chochokera mu mtima mwake,
3 ndipo m'kamwa mwake simutuluka mawu osinjirira,
amene sachitira choyipa mnansi wake
kapena kufalitsa mbiri yoyipa ya munthu mnzake,
4 amene sapereka ulemu kwa munthu woyipa.
Koma amalemekeza amene amaopa Yehova,
amene amakwaniritsa zomwe walonjeza
ngakhale pamene zikumupweteka,
5 amene amakongoletsa ndalama zake popanda chiwongoladzanja
ndipo salandira chiphuphu pofuna kutsutsa anthu osalakwa.

Iye amene amachita zinthu zimenezi
sadzagwedezeka konse.

# Salimo 16

Mikitamu ya Davide.
1 Ndisungeni Inu Mulungu,
pakuti ine ndimathawira kwa Inu.

2 Ndinati kwa Yehova, "Inu ndinu Ambuye anga;
popanda Inu, ine ndilibe chinthu chinanso chabwino."
3 Kunena za oyera mtima amene ali pa dziko,
amenewa ndi olemekezeka, amene ndimakondwera nawo.
4 Anthu amene amathamangira kwa milungu ina
mavuto awo adzachulukadi.
Ine sindidzathira nawo nsembe zawo zamagazi
kapena kutchula mayina awo ndi pakamwa panga.

5 Yehova, Inu mwandipatsa cholowa changa ndi chikho changa;
mwateteza kolimba gawo langa.
6 Malire a malo anga akhala pabwino;
ndithudi, ine ndili cholowa chokondweretsa kwambiri.

7 Ine ndidzatamanda Yehova amene amandipatsa uphungu;
ngakhale usiku mtima wanga umandilangiza.
8 Ndayika Yehova patsogolo panga nthawi zonse.
Popeza Iyeyo ali kudzanja langa lamanja,
sindidzagwedezeka.

9 Choncho mtima wanga ndi wosangalala ndipo pakamwa panga pakukondwera;
thupi langanso lidzakhala pabwino,
10 chifukwa Inu simudzandisiya ku manda,
simudzalola kuti woyera wanu avunde.
11 Inu mwandidziwitsa njira ya moyo;
mudzandidzaza ndi chimwemwe pamaso panu,
ndidzasangalala mpaka muyaya pa dzanja lanu lamanja.

# Salimo 17

Pemphero la Davide.
1 Imvani Inu Yehova pempho langa lachilungamo;
mverani kulira kwanga.
Tcherani khutu kuti mumve pemphero langa
popeza silikuchokera pakamwa pachinyengo.
2 Kusalakwa kwanga kuchokera kwa inu;
maso anu aone chimene ndi cholungama.

3 Ngakhale Inu mutafufuza mtima wanga ndi kundisanthula usiku,
ngakhale mutandiyesa, simudzapeza kanthu;
Ine ndatsimikiza kuti pakamwa panga sipadzachimwa.
4 Kunena za ntchito za anthu,
monga mwa mawu a pakamwa panu,
Ine ndadzisunga ndekha
posatsata njira zachiwawa.
5 Mayendedwe anga akhazikika pa njira zanu;
mapazi anga sanaterereke.

6 Ine ndikuyitana Inu, Mulungu wanga, pakuti mudzandiyankha;
tcherani khutu lanu kwa ine ndipo mumve pemphero langa.
7 Onetsani kudabwitsa kwa chikondi chanu chachikulu,
Inu amene mumapulumutsa ndi dzanja lanu lamanja
iwo amene amathawira kwa inu kuchoka kwa adani awo.
8 Mundisunge ine ngati mwanadiso;
mundibise mu mthunzi wa mapiko anu,
9 kuchoka kwa oyipa amene amandizinga ine,
kuchoka kwa anthu amene ndi adani anga, amene andizungulira ine.

10 Iwo amatseka mitima yawo yopanda chifundo,
ndi pakamwa pawo amayankhula modzitamandira.
11 Andisaka, tsopano andizungulira
ndi maso awo atcheru, kuti andigwetse pansi.
12 Iwo ali ngati mkango wofuna nyama;
ngati mkango waukulu wokhala mobisala.

13 Dzukani Yehova, mulimbane nawo ndipo muwagwetse pansi;
landitseni kuchoka kwa oyipa ndi lupanga lanu.
14 Inu Yehova, pulumutseni ndi dzanja lanu kwa anthu otere,
kwa anthu a dziko lino amene mphotho yawo ili m'moyo uno.

Inu mumaletsa njala kwa amene asangalatsidwa nanu;
ana awo aamuna ali ndi zinthu zambiri,

ndipo iwo amasunga chuma cha ana awo.
15 Ndipo ine m'chilungamo ndidzaona nkhope yanu;
pamene ndidzadzuka, ndidzakondwera kwambiri poonana nanu.

# Salimo 18

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide mtumiki wa Yehova. Iye anayimbira Yehova nyimbo iyi pamene Yehovayo anamupulumutsa m'dzanja la adani ake onse ndiponso m'dzanja la Sauli.

1 Davide anati: Ine ndimakukondani Inu Yehova, mphamvu zanga.

2 Yehova ndiye thanthwe langa, chitetezo changa ndi mpulumutsi wanga;
Mulungu wanga ndi thanthwe langa m'mene ndimathawiramo.
Chishango changa ndi ndodo yachipulumutso changa, ndi linga langa.
3 Ndimayitana Yehova amene ndi woyenera matamando,
ndipo ndapulumutsidwa kwa adani anga.

4 Zingwe za imfa zinandizinga;
mitsinje yothamanga yachiwonongeko inandiopsa kwambiri.
5 Anandimanga ndi zingwe za ku manda;
misampha ya imfa inalimbana nane.
6 M'masautso anga ndinapemphera kwa Yehova;
ndinalirira kwa Mulungu wanga kuti andithandize.
Ali m'Nyumba yake, anamva mawu anga;
kulira kwanga kunafika pamaso pake ndi m'makutu mwake.

7 Dziko lapansi linanjenjemera ndi kuchita chivomerezi,
ndipo maziko a mapiri anagwedezeka;
ananjenjemera chifukwa Iye anakwiya.
8 M'mphuno mwake munatuluka utsi;
moto wonyeketsa unatuluka m'kamwa mwake,
makala amoto anali lawilawi m'kamwa mwake.
9 Iye anang'amba thambo natsika pansi;
pansi pa mapazi ake panali mitambo yakuda.
10 Iye anakwera pa Kerubi ndi kuwuluka;
nawuluka ndi mphepo mwaliwiro.
11 Iye anapanga mdima kukhala chofunda chake,
chophimba chake chomuzungulira chinali mitambo yakuda ya mlengalenga.
12 M'kuwala kumene kunali pamaso pake munkachokera matalala,
makala amoto ndi ziphaliwali zong'anima.
13 Yehova anabangula kumwamba ngati bingu,
mawu a Wammwambamwamba anamveka ponseponse.
14 Iye anaponya mivi yake nabalalitsa adani ake,
ndi zing'aning'ani zake anawagonjetsa.
15 Zigwa za m'nyanja zinaonekera poyera;
maziko a dziko lapansi anakhala poyera,
Yehova atabangula mwaukali,
pamene mpweya wamphamvu unatuluka m'mphuno mwanu.

16 Ali kumwamba, Iye anatambalitsa dzanja lake ndipo anandigwira;
anandivuwula m'madzi ozama.
17 Anandipulumutsa kwa mdani wanga wamphamvu,

adani anga, amene anali amphamvu kuposa ine.
18 Adaniwo analimbana nane pamene ndinali pa mavuto,
koma Yehova anali thandizo langa.
19 Iye anandipititsa kumalo otakasuka;
anandipulumutsa chifukwa amakondwera nane.

20 Yehova wandithandiza molingana ndi chilungamo changa;
molingana ndi makhalidwe anga abwino, Iye wandipulumutsa.
21 Pakuti ine ndinatsata njira za Yehova;
ndilibe mlandu wochoka pamaso Mulungu wanga.
22 Malamulo ake onse ali pamaso panga;
sindinasiye malangizo ake.
23 Ndakhala moyo wosalakwa pamaso pake
ndipo ndakhala ndi kupewa tchimo.
24 Yehova wandipatsa mphotho molingana ndi chilungamo changa,
molingana ndi kuyera kwa manja anga pamaso pake.

25 Kwa wokhulupirika, Inu mumaonetsa kukhulupirika kwanu;
kwa anthu amakhalidwe abwino, Inu mumaonetsanso makhalidwe abwino,
26 kwa woyera mtima, Inu mumaonetsa kuyera mtima kwanu,
koma kwa achinyengo mumaonetsanso kunyansidwa nawo.
27 Inu mumapulumutsa anthu odzichepetsa,
koma anthu amtima odzikuza mumawatsitsa.
28 Inu Yehova, sungani nyale yanga kuti iziyakabe;
Mulungu wanga wasandutsa mdima wanga kukhala kuwunika.
29 Ndi thandizo lanu nditha kulimbana ndi gulu la ankhondo;
ndi Mulungu wanga nditha kuchita zosatheka ndi munthu.

30 Kunena za Mulungu, zochita zake ndi zangwiro;
mawu a Yehova alibe cholakwika.
Iye ndi chishango
kwa onse amene amathawira kwa Iye.
31 Mulungu wina ndi uti wofanana nanu Yehova?
Ndipo ndani amene ndi Thanthwe kupatula Mulungu wathu?
32 Ndi Mulungu amene anandipatsa mphamvu
ndi kulungamitsa njira yanga.
33 Iye amasandutsa mapazi anga kukhala ngati ambawala yayikazi;
Iye amandithandiza kuyimirira pamwamba pa mapiri.
34 Iye amaphunzitsa manja anga kuchita nkhondo;
manja anga amatha kuthyola uta wachitsulo.
35 Inu mumandipatsa chishango chachipambano,
ndipo dzanja lanu lamanja limandichirikiza;
mumawerama pansi kundikuza.
36 Munakulitsa njira yoyendamo ine,
kuti mapazi anga asaguluke.

37 Ndinathamangitsa adani anga ndi kuwapitirira;
sindinabwerere mpaka atawonongedwa.
38 Ndinakantha adaniwo kotero kuti sanathenso kudzuka;
anagwera pa mapazi anga.
39 Inu munandiveka ndi mphamvu yokachitira nkhondo,

munachititsa kuti ndigonjetse adani anga.
40 Inu munachititsa adani anga kutembenuka, kuonetsa misana yawo pothawa,
ndipo ine ndinawononga adani angawo.
41 Iwo anafuwula kupempha thandizo, koma panalibe ndi mmodzi yemwe owapulumutsa.
Analirira kwa Yehova koma sanawayankhe.
42 Ine ndinawaperesa ngati fumbi lowuluka ndi mphepo.
Ndinawapondaponda ngati matope a m'misewu.

43 Inu mwandipulumutsa m'manja mwa anthu;
mwandisandutsa kukhala mtsogoleri wa anthu a mitundu ina.
Anthu amene sindikuwadziwa ali pansi pa ulamuliro wanga.
44 Alendo amadzipereka okha pamaso panga;
akangomva za ine amandigonjera.
45 Iwo onse anataya mtima;
anatuluka m'malinga awo akunjenjemera.

46 Yehova ndi wamoyo! Litamandidwe Thanthwe langa!
Akuzike Mulungu Mpulumutsi wanga!
47 Iye ndi Mulungu amene amabwezera chilango,
amene amagonjetsa anthu a mitundu yonse amene ali pansi pa ulamuliro wanga,
48 amene amandipulumutsa m'manja mwa adani anga.
Inu munandikuza kuposa adani anga;
munandilanditsa m'manja mwa anthu ankhanza.
49 Choncho ine ndidzakutamandani pakati pa anthu a mitundu ina, Inu Yehova;
ndidzayimba nyimbo zotamanda dzina lanu.
50 Iye amapereka chipambano chachikulu kwa mfumu yake;
amaonetsa chikondi chosasinthika kwa wodzozedwa wake,
kwa Davide ndi zidzukulu zake kwamuyaya.

# Salimo 19

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Zakumwamba zimalengeza za ulemerero wa Mulungu;
thambo limalalikira ntchito za manja ake.
2 Tsiku ndi tsiku zimayankhula mawu ambiri,
usiku ndi usiku zimaonetsa poyera nzeru.
3 Palibe kuyankhula, palibe mawu aliwonse;
liwu lawo silimveka.
4 Koma uthenga wawo umapita pa dziko lonse lapansi,
mawuwo amafika mpaka
kumalekezero a dziko lapansi.
5 Dzuwa lili ngati mkwatibwi wobwera kuchokera ku nsanja yake,
ngati katswiri wokondwerera kuthamanga pa mpikisano.
6 Limatuluka kuyambira mbali ina ya thambo
ndi kuzungulira mpaka mbali inanso;
palibe chinthu chotha kupewa kutentha kwake.

7 Lamulo la Yehova ndi langwiro,
kutsitsimutsa moyo.

Maumboni a Yehova ndi odalirika,
amapereka nzeru kwa wopanda nzeru.
8 Malangizo a Yehova ndi olungama,
amapereka chimwemwe mu mtima.
Malamulo a Yehova ndi onyezimira,
amapereka kuwala.
9 Kuopa Yehova ndiye chinthu changwiro,
chimakhala mpaka muyaya.
Maweruzo a Yehova ndi owona
ndipo onse ndi olungama;
10 ndi a mtengowapatali kuposa golide,
kuposa golide weniweni;
ndi otsekemera kuposa uchi,
kuposa uchi wochokera pa chisa chake.
11 Mtumiki wanu amachenjezedwa nawo;
powasunga pali mphotho yayikulu.

12 Ndani angathe kudziwa zolakwa zake?
Mundikhululukire zolakwa zanga zobisika.
13 Muteteze mtumiki wanunso ku machimo ochita akudziwa;
iwo asandilamulire.
Kotero ndidzakhala wosalakwa,
wopanda mlandu wa tchimo lalikulu.

14 Mawu a m'kamwa mwanga ndi zolingalira za mu mtima mwanga
zikhale zokondweretsa pamaso panu,
Inu Yehova, Thanthwe langa ndi Mpulumutsi wanga.

# Salimo 20

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Yehova akuyankhe pamene uli pa msautso;
dzina la Mulungu wa Yakobo likuteteze.
2 Iye atumize thandizo kuchokera ku malo ake opatulika;
akugwirizize kuchokera ku Ziyoni.
3 Iye akumbukire nsembe zako zonse
ndipo alandire nsembe zako zopsereza.
Sela
4 Akupatse chokhumba cha mtima wako
ndipo akuthandize kuti zonse wakonza zichitike.
5 Ife tidzafuwula ndi chimwemwe pamene iwe wapambana
ndipo tidzanyamula mbendera zathu m'dzina la Mulungu wathu,
Yehova ayankhe zopempha zako zonse.

6 Tsopano ndadziwa kuti Yehova amapulumutsa wodzozedwa wake;
Iye amamuyankha kuchokera kumwamba ku malo ake opatulika
ndi mphamvu yopulumutsa ya dzanja lake lamanja.
7 Ena amadalira magaleta ndipo ena akavalo
koma ife tidzadalira dzina la Yehova Mulungu wathu.
8 Iwo amagonjetsedwa ndi kugwa,
koma ife timadzuka ndi kuyima chilili.

9 Inu Yehova, pulumutsani mfumu!

Tiyankheni pamene tikuyitanani!

# Salimo 21

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Inu Yehova, mfumu ikusangalala mu mphamvu yanu,
chimwemwe chake n'chachikuludi pa kupambana kumene mumapereka!
2 Inu mwayipatsa zokhumba za mtima wake
ndipo simunayimane zopempha za pa milomo yake.
Sela
3 Inu munayilandira ndi madalitso ochuluka
ndipo munayiveka chipewa chaufumu chagolide weniweni pa mutu wake.
4 Iye anakupemphani moyo, ndipo munamupatsa
masiku ochuluka kwamuyaya.
5 Kudzera m'zigonjetso zimene munapereka, ulemerero wake ndi waukulu;
Inu mwapereka pa iyo ulemerero ndi ufumu.
6 Zoonadi Inu mwayipatsa madalitso amuyaya,
Inu mwayipatsa chisangalalo ndi chimwemwe chimene chili pamaso panu.
7 Pakuti mfumu imadalira Yehova;
kudzera m'chikondi chake chosatha cha Wammwambamwamba,
iyo sidzagwedezeka.

8 Dzanja lanu lidzayimitsa adani anu onse;
dzanja lanu lamanja lidzagwira adani anu.
9 Pa nthawi ya kuonekera kwanu
mudzawasandutsa ng'anjo yamoto yotentha.
Mu ukali wake Yehova adzawameza,
ndipo moto wake udzawatha.
10 Inu mudzawononga ana awo pa dziko lapansi,
zidzukulu zawo pakati pa anthu.
11 Ngakhale iwo akukonzereni chiwembu mwa kuchenjera kwawo
sadzapambana;
12 pakuti mudzawapirikitsa ndipo adzaonetsa misana yawo
pamene mudzawaloza ndi mivi yanu.

13 Mukwezeke Inu Yehova m'mphamvu yanu,
ife tidzayimba nyimbo ndi kutamanda mphamvu yanu.

# Salimo 22

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Monga mwa "Mbawala yayikazi ya Mmawa." Salimo la Davide.
1 Mulungu wanga, Mulungu wanga, n'chifukwa chiyani mwandisiya?
Chifuwa chiyani simukundithandiza ndi pang'ono pomwe?
N'chifukwa chiyani simukumva mawu a kudandaula kwanga?
2 Inu Mulungu wanga, ine ndimalira masana, koma simuyankha,
usikunso, ndipo sindikhala chete.

3 Inu ndinu Woyera, wokhala pa mpando waufumu;
ndinu matamando a Israeli.

4 Pa inu makolo athu anadalira;
iwo anadalira ndipo Inu munawapulumutsa.
5 Analirira kwa inu ndipo munawapulumutsa.
Iwo anakhulupirira Inu ndipo simunawakhumudwitse.

6 Koma ine ndine nyongolotsi osati munthu,
wosekedwa ndi wonyozedwa ndi anthu onse.
7 Onse amene amandiona amandiseka;
amandiyankhulira mawu achipongwe akupukusa mitu yawo kunena kuti
8 "Iyeyu amadalira Yehova,
musiyeni Yehovayo amulanditse.
Musiyeni Yehova amupulumutse
popeza amakondwera mwa Yehovayo."

9 Komabe Inu ndinu amene munandibadwitsa, munanditulutsa m'mimba mwa amayi anga.
Munachititsa kuti ndizikudalirani
ngakhale pa nthawi imene ndinkayamwa.
10 Chibadwire ine ndinaperekedwa kwa Inu;
kuchokera m'mimba mwa amayi anga Inu mwakhala muli Mulungu wanga.
11 Musakhale kutali ndi ine,
pakuti mavuto ali pafupi
ndipo palibe wina wondipulumutsa.

12 Ng'ombe zazimuna zandizungulira;
ng'ombe zazimuna zamphamvu za ku Basani zandizinga.
13 Mikango yobangula pokadzula nyama,
yatsekula kwambiri pakamwa pawo kulimbana nane.
14 Ine ndatayika pansi ngati madzi
ndipo mafupa anga onse achoka m'malo mwake.
Mtima wanga wasanduka phula;
wasungunuka m'kati mwanga.
15 Mphamvu zanga zauma ngati phale,
ndipo lilime langa lamamatira ku nsagwada;
mwandigoneka m'fumbi la imfa.
16 Agalu andizungulira;
gulu la anthu oyipa landizinga.
Alasa manja ndi mapazi anga.
17 Ine nditha kuwerenga mafupa anga onse;
anthu amandiyang'anitsitsa ndi kundidzuma.
18 Iwo agawana zovala zanga pakati pawo
ndi kuchita maere pa zovala zangazo.

19 Koma Inu Yehova, musakhale kutali;
Inu mphamvu yanga, bwerani msanga kuti mudzandithandize.
20 Pulumutsani moyo wanga ku lupanga,
moyo wanga wopambanawu ku mphamvu ya agalu.
21 Ndilanditseni m'kamwa mwa mikango;
pulumutseni ku nyanga za njati.

22 Ine ndidzalengeza dzina lanu kwa abale anga;
ndidzakutamandani mu msonkhano.
23 Inu amene mumaopa Yehova mutamandeni!
Inu zidzukulu zonse za Yakobo, mulemekezeni!
Muopeni mwaulemu, inu zidzukulu zonse za Israeli!
24 Pakuti Iye sanapeputse kapena kunyoza
kuvutika kwa wosautsidwayo;
Iye sanabise nkhope yake kwa iye.
Koma anamvera kulira kwake kofuna thandizo.

25 Ndidzakutamandani pa msonkhano waukulu chifukwa cha zimene mwandichitira.
Ndidzakwaniritsa lonjezo langa pamaso pa amene amaopa Inu.
26 Osauka adzadya ndipo adzakhuta;
iwo amene amafunafuna Yehova adzamutamanda.
Mitima yanu ikhale ndi moyo mpaka muyaya!
27 Malekezero onse a dziko lapansi
adzakumbukira Yehova ndi kutembenukira kwa Iye,
ndipo mabanja a mitundu ya anthu
adzawerama pamaso pake,
28 pakuti ulamuliro ndi wake wa Yehova
ndipo Iye amalamulira anthu a mitundu yonse.

29 Anthu olemera onse a dziko lapansi adzachita phwando ndi kulambira;
onse amene amapita ku fumbi adzagwada pamaso pake;
iwo amene sangathe kudzisunga okha ndi moyo.
30 Zidzukulu zam'tsogolo zidzamutumikira Iye;
mibado ya m'tsogolo idzawuzidwa za Ambuye.
31 Iwo adzalengeza za chilungamo chake
kwa anthu amene pano sanabadwe
pakuti Iye wachita zimenezi.

# Salimo 23

Salimo la Davide.
1 Yehova ndiye m'busa wanga, sindidzasowa kanthu.
2 Amandigoneka pa msipu wobiriwira,
amanditsogolera ku madzi akumwa abwino,
3 amatsitsimutsa moyo wanga.
Amanditsogolera m'njira zachilungamo
chifukwa cha dzina lake.
4 Ngakhale ndiyende
m'chigwa cha mdima wakuda bii,
sindidzaopa choyipa,
pakuti Inu muli ndi ine;
chibonga chanu ndi ndodo yanu
zimanditonthoza.

5 Mumandikonzera chakudya
adani anga akuona.
Mumadzoza mutu wanga ndi mafuta;
chikho changa chimasefukira.
6 Zoonadi, zokoma ndi chikondi chosasinthika zidzanditsata

masiku onse a moyo wanga,
ndipo ndidzakhala m’Nyumba ya Yehova
kwamuyaya.

# Salimo 24

Salimo la Davide.
1 Dziko lapansi ndi la Yehova ndi zonse zimene zili m’menemo,
dziko ndi onse amene amakhala m’menemo;
2 pakuti Iye ndiye anayika maziko ake pa nyanja
ndi kulikhazika pamwamba pa madzi.

3 Ndani angakwere phiri la Yehova?
Ndani angathe kuyima pa malo ake opatulika?
4 Iye amene ali ndi m’manja moyera ndi mtima woyera,
amene sapereka moyo wake kwa fano
kapena kulumbira mwachinyengo.
5 Iyeyo adzalandira madalitso kwa Yehova
ndipo Mulungu mpulumutsi wake adzagamula kuti alibe mlandu.
6 Umenewo ndiwo m’bado wa amene amafunafuna Yehova;
amene amafunafuna nkhope yanu, Inu Mulungu wa Yakobo.
Sela

7 Tukulani mitu yanu inu zipata;
tsekukani, inu zitseko zakalekalenu,
kuti Mfumu yaulemerero ilowe.
8 Kodi Mfumu yaulemereroyo ndani?
Yehova Wamphamvuzonse,
Yehova ndiye wamphamvu pa nkhondo.
9 Tukulani mitu yanu, inu zipata;
tsekukani, inu zitseko zakalekalenu,
kuti Mfumu yaulemerero ilowe.
10 Kodi Mfumu yaulemereroyo ndani?
Yehova Wamphamvuzonse,
Iye ndiye Mfumu yaulemerero.
Sela

# Salimo 25

Salimo la Davide.
1 Kwa Inu Yehova, ndipereka moyo wanga.
2 Ndimadalira Inu Mulungu wanga.
Musalole kuti ndichite manyazi
kapena kuti adani anga andipambane.
3 Aliyense amene amayembekezera kwa Ambuye
sadzachititsidwa manyazi
koma achinyengo ndiwo adzachititsidwe manyazi
ndipo sadzakhala ndi chodzitetezera.

4 Ndidziwitseni njira zanu Inu Yehova,
phunzitseni mayendedwe anu;
5 tsogolereni m’choonadi chanu ndi kundiphunzitsa,
pakuti Inu ndinu Mulungu mpulumutsi wanga,
ndipo chiyembekezo changa chili mwa Inu tsiku lonse.

6 Kumbukirani Inu Yehova chifundo ndi chikondi chanu chachikulu,
pakuti ndi zakalekale.
7 Musakumbukire machimo a ubwana wanga
ndi makhalidwe anga owukira;
molingana ndi chikondi chanu ndikumbukireni ine,
pakuti Inu Yehova ndinu wabwino.

8 Yehova ndi wabwino ndi wolungama;
choncho Iye akulangiza ochimwa m'njira yake.
9 Amatsogolera odzichepetsa kuti achite zolungama
ndipo amawaphunzitsa njira zake.
10 Njira zonse za Yehova ndi zachikondi ndi zokhulupirika
kwa iwo amene amasunga zofuna za pangano lake.
11 Chifukwa cha dzina lanu, Inu Yehova,
khululukireni mphulupulu zanga, ngakhale kuti ndi zochuluka.
12 Tsono ndani munthu amene amaopa Yehova?
Yehova adzamulangiza njira yoti ayitsate.
13 Iye adzakhala pa ulemerero masiku ake onse,
ndipo zidzukulu zake zidzalandira dziko ngati cholowa chawo.
14 Yehova amawulula chinsinsi chake kwa iwo amene amamuopa;
amawulula pangano lake kwa iwowo.
15 Maso anga ali pa Yehova nthawi zonse,
pakuti ndi Iye yekha amene adzawonjola mapazi anga mu msampha.

16 Tembenukirani kwa ine ndipo mundikomere mtima,
pakuti ndili ndekhandekha ndipo ndikuzunzika.
17 Masautso a mu mtima mwanga achulukirachulukira;
masuleni ku zowawa zanga.
18 Penyani mazunzo anga ndi zovuta zanga
ndipo mufafanize machimo anga onse.
19 Onani mmene adani anga achulukira
ndi momwe chidani chawo ndi ine chakulira.
20 Tetezani moyo wanga ndi kundilanditsa;
musalole kuti ndichite manyazi,
pakuti ndimathawira kwa Inu.
21 Kukhulupirika ndi kulungama kwanga kunditeteze,
chifukwa chiyembekezo changa chili mwa Inu.

22 Wombolani Israeli Inu Mulungu,
ku mavuto ake onse!

# Salimo 26

Salimo la Davide.
1 Weruzeni Inu Yehova
pakuti ndakhala moyo wosalakwa.
Ndadalira Yehova
popanda kugwedezeka.
2 Patseni mayeso, Inu Yehova ndipo ndiyeseni,
santhulani mtima wanga ndi maganizo anga;
3 pakuti chikondi chanu chili pamaso panga nthawi zonse,
ndipo ndimayenda m'choonadi chanu nthawi zonse.
4 Ine sindikhala pansi pamodzi ndi anthu achinyengo,

kapena kufunsa nzeru kwa achiphamaso.
5 Ndimanyansidwa ndi msonkhano wa anthu ochita zoyipa
ndipo ndimakana kukhala pansi pamodzi ndi oyipa.
6 Ndimasamba m'manja mwanga kuonetsa kusalakwa kwanga
ndi kupita kukatumikira pa guwa lanu la nsembe, Inu Yehova,
7 kulengeza mofuwula za matamando anu
ndi kuwuza onse za ntchito zanu zodabwitsa.
8 Ndimakonda Nyumba imene Inu Yehova mumakhalamo,
malo amene ulemerero wanu umapezekako.

9 Musachotse moyo wanga pamodzi ndi ochimwa,
moyo wanga pamodzi ndi anthu akupha anzawo,
10 amene m'manja mwawo muli ndondomeko zoyipa,
dzanja lawo lamanja ladzaza ndi ziphuphu.
11 Koma ine ndimakhala moyo wosalakwa;
mu msonkhano wa anthu anu ndidzatamanda Yehova.

12 Ndayima pa malo wopanda zovuta
ndipo ndidzatamanda Yehova mu msonkhano waukulu.

# Salimo 27

Salimo la Davide.
1 Yehova ndiye kuwunika kwanga ndi chipulumutso changa;
ndidzaopa yani?
Yehova ndi linga la moyo wanga;
ndidzachita mantha ndi yani?
2 Pamene anthu oyipa abwera kudzalimbana nane
kudzadya mnofu wanga,
pamene adani anga ndi achiwembu andithira nkhondo,
iwo adzapunthwa ndi kugwa.
3 Ngakhale gulu lankhondo lindizinge,
mtima wanga sudzaopa.
Ngakhale nkhondo itayambika kulimbana nane,
ngakhale nthawi imeneyo, ine ndidzalimbika mtima.

4 Chinthu chimodzi chokha chimene ndipempha kwa Yehova,
ichi ndi chimene ndidzachifunafuna:
kuti ndikhale m'Nyumba ya Yehova
masiku onse a moyo wanga,
ndi kuyang'ana kukongola kwa Yehova,
ndi kumufunafuna Iye m'Nyumba yake.
5 Pakuti pa tsiku la msautso
Iye adzanditeteza m'malo ake okhalamo;
adzandibisa m'kati mwa Nyumba yake
ndi kukhazika ine pamwamba pa thanthwe.
6 Kotero mutu wanga udzakwezedwa
kuposa adani anga amene andizungulira;
pa Nyumba yake ndidzapereka nsembe ndi mfuwu wachimwemwe;
ndidzayimba nyimbo kwa Yehova.

7 Imvani mawu anga pamene ndiyitana Inu Yehova
mundichitire chifundo ndipo mundiyankhe.

8 Mtima wanga ukuti kwa Inu, “Funafuna nkhope yake!”
Nkhope yanu Yehova ndidzayifunafuna.
9 Musandibisire nkhope yanu,
musamubweze mtumiki wanu mwamkwiyo;
mwakhala muli thandizo langa.
Musandikane kapena kunditaya,
Inu Mulungu Mpulumutsi wanga.
10 Ngakhale abambo ndi amayi anga anditaya
Yehova adzandisamala.
11 Phunzitseni njira yanu Inu Yehova,
munditsogolere m’njira yowongoka
chifukwa cha ondizunza.
12 Musandipereke ku zokhumba za adani anga,
pakuti mboni zambiri zauka kutsutsana nane
ndipo zikundiopseza.

13 Ine ndikutsimikiza mtima za zimenezi;
ndidzaona ubwino wa Yehova
m’dziko la anthu amoyo.
14 Dikirani pa Yehova;
khalani anyonga ndipo limbani mtima
nimudikire Yehova.

# Salimo 28

Salimo la Davide.
1 Kwa Inu ine ndiyitana, Yehova ndinu Thanthwe langa;
musakhale osamva kwa ine.
Pakuti mukapitirira kukhala chete,
ndidzakhala ngati iwo amene atsikira ku dzenje.
2 Imvani kupempha chifundo kwanga
pomwe ndikuyitana kwa Inu kuti mundithandize,
pomwe ndikukweza manja anga
kuloza ku malo anu oyeretsetsa.

3 Musandikokere kutali pamodzi ndi anthu oyipa,
pamodzi ndi iwo amene amachita zoyipa,
amene amayankhula mwachikondi ndi anzawo
koma akusunga chiwembu m’mitima mwawo.
4 Muwabwezere chifukwa cha zochita zawo
ndi ntchito zawo zoyipa;
abwezereni chifuwa cha zimene manja awo achita
ndipo mubweretse pa iwo zimene zowayenera.
5 Popeza iwowo sakhudzidwa ndi ntchito za Yehova,
ndi zimene manja ake anazichita,
Iye adzawakhadzula
ndipo sadzawathandizanso.

6 Matamando apite kwa Yehova,
popeza Iye wamva kupempha chifundo kwanga.
7 Yehova ndiye mphamvu yanga ndi chishango changa;
mtima wanga umadalira Iye, ndipo Ine ndathandizidwa.
Mtima wanga umalumphalumpha chifukwa cha chimwemwe
ndipo ndidzayamika Iye m’nyimbo.

8 Yehova ndi mphamvu ya anthu ake,
linga la chipulumutso kwa wodzozedwa wake.
9 Pulumutsani anthu anu ndipo mudalitse cholowa chanu;
mukhale m’busa wawo ndipo muwakweze kwamuyaya.

# Salimo 29

Salimo la Davide.
1 Perekani kwa Yehova, inu anthu amphamvu,
perekani kwa Yehova ulemerero ndi mphamvu.
2 Perekani kwa Yehova ulemerero woyenera dzina lake,
pembedzani Yehova mwa kukongola kwa chiyero chake.

3 Liwu la Yehova lili pamwamba pa madzi;
Mulungu waulemerero abangula,
Yehova abangula pamwamba pa madzi amphamvu.
4 Liwu la Yehova ndi lamphamvu;
liwu la Yehova ndi laulemerero.
5 Liwu la Yehova limathyola mikungudza;
Yehova amathyolathyola mikungudza ya ku Lebanoni.
6 Iye amachititsa Lebanoni kulumphalumpha ngati mwana wang’ombe,
Siriyoni ngati mwana wa njati:
7 Liwu la Yehova limakantha
ngati kung’anima kwa mphenzi.
8 Liwu la Yehova limagwedeza chipululu;
Yehova amagwedeza chipululu cha Kadesi.
9 Liwu la Yehova limapindapinda mibawa
ndi kuyeretsa nkhalango.
Ndipo m’Nyumba mwake onse amafuwula kuti, “Ulemerero!”

10 Yehova amakhala pamwamba pa madzi osefukira,
Yehova ndiye mfumu kwamuyaya.
11 Yehova amapereka mphamvu kwa anthu ake;
Yehova amadalitsa anthu ake ndi mtendere.

# Salimo 30

Salimo la Davide. Nyimbo yoyimba popereka Nyumba ya Mulungu.
1 Ndidzakukwezani Yehova,
chifukwa mwanditulutsa kwakuya,
ndipo simunalole kuti adani anga akondwere pa ine.
2 Inu Yehova Mulungu wanga ndinapempha kwa Inu thandizo
ndipo Inu munandichiritsa.
3 Inu Yehova, munanditulutsa ku manda,
munandisunga kuti ndisatsalire m’dzenje.

4 Imbirani Yehova inu anthu ake okhulupirika;
tamandani dzina lake loyera.
5 Pakuti mkwiyo wake umakhala kwa kanthawi
koma kukoma mtima kwake ndi kwa moyo wonse;
utha kuchezera kulira usiku wonse,
koma chimwemwe chimabwera mmawa.

6 Pamene ndinaona kuti ndili otetezedwa ndinati,

"Sindidzagwedezekanso."
7 Inu Yehova, pamene munandikomera mtima,
munachititsa phiri langa kuyima chilili;
koma pamene munabisa nkhope yanu,
ndinataya mtima.

8 Kwa Inu Yehova ndinayitana;
kwa Ambuye ndinapempha chifundo;
9 "Kodi pali phindu lanji powonongeka kwanga
ngati nditsikira ku dzenje?
Kodi fumbi lidzakutamandani Inu?
Kodi lidzalengeza za kukhulupirika kwanu?
10 Imvani Yehova ndipo mundichitire chifundo;
Yehova mukhale thandizo langa."

11 Inu munasandutsa kulira kwanga kukhala kuvina;
munachotsa chiguduli changa ndi kundiveka ndi chimwemwe,
12 kuti mtima wanga uthe kuyimbira Inu usakhale chete.
Yehova Mulungu wanga, ndidzapereka kwa Inu mayamiko kwamuyaya.

# Salimo 31

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Mwa Inu Yehova, ine ndimathawiramo;
musalole n'komwe kuti ndichititsidwe manyazi;
mundipulumutse chifukwa cha chilungamo chanu.
2 Tcherani khutu lanu kwa ine,
bwerani msanga kudzandilanditsa;
mukhale thanthwe langa lothawirapo,
linga lolimba kundipulumutsa ine.
3 Popeza Inu ndinu thanthwe langa ndi linga langa,
chifukwa cha dzina lanu tsogolereni ndi kundiwongolera.
4 Ndimasuleni mu msampha umene anditchera
pakuti ndinu pothawirapo panga.
5 M'manja mwanu ndipereka mzimu wanga;
womboleni Yehova Mulungu wachoonadi.

6 Koma ine ndimadana nawo amene amamamatira mafano achabechabe;
ine ndimadalira Yehova.
7 Ndidzakondwa ndi kusangalala m'chikondi chanu
popeza Inu munaona masautso anga
ndipo mumadziwa kuwawa kwa moyo wanga.
8 Inu simunandipereke kwa mdani
koma mwayika mapazi anga pa malo otakasuka.

9 Mundichitire chifundo Inu Yehova pakuti ndili pa mavuto;
maso anga akulefuka ndi chisoni,
m'moyo mwanga ndi m'thupi mwanga momwe mukupweteka.
10 Moyo wanga ukunyeka chifukwa cha kuwawidwa mtima
ndi zaka zanga chifukwa cha kubuwula;
mphamvu zanga zatha chifukwa cha masautso,

ndipo mafupa anga akulefuka.
11 Chifukwa cha adani anga onse,
ndine wonyozeka kwambiri ndi anansi anga;
ndine chochititsa manyazi kwa abwenzi anga.
Iwo amene amandiona mu msewu amandithawa.
12 Ine ndinayiwalika kwa iwo ngati kuti ndinamwalira;
ndakhala ngati m'phika wosweka.
13 Pakuti ine ndamva zonena zoyipa za anthu ambiri;
zoopsa zandizungulira mbali zonse;
iwo akukonza chiwembu kuti alimbane nane,
kuti atenge moyo wanga.

14 Koma ndikudalira Inu Yehova;
ndikunena kuti, "Ndinu Mulungu wanga."
15 Masiku anga ali m'manja mwanu;
ndipulumutseni kwa adani anga
ndi kwa iwo amene akundithamangitsa.
16 Walitsani nkhope yanu pa mtumiki wanu;
pulumutseni mwa chikondi chanu chosatha.
17 Yehova musalole kuti ndichite manyazi,
pakuti ndalirira kwa Inu;
koma oyipa achititsidwe manyazi
ndipo agone chete m'manda.
18 Milomo yawo yabodzayo ikhale chete,
pakuti chifukwa cha kunyada
ayankhula modzikuza kutsutsana ndi wolungama.

19 Ndi waukulu ubwino wanu
umene mwawasungira amene amakuopani,
umene mumapereka anthu akuona
kwa iwo amene amathawira kwa Inu.
20 Mu mthunzi wa pamalo popezeka panu muwabisa,
kuwateteza ku ziwembu za anthu;
m'malo anu okhalamo mumawateteza
kwa anthu owatsutsa.

21 Matamando akhale kwa Yehova,
pakuti anaonetsa chikondi chake chodabwitsa kwa ine
pamene ndinali mu mzinda wozingidwa.
22 Ndili m'nkhawa zanga ndinati,
"Ine ndachotsedwa pamaso panu!"
Komabe Inu munamva kupempha chifundo kwanga
pamene ndinapempha thandizo kwa Inu.

23 Kondani Yehova oyera mtima ake onse!
Yehova amasunga wokhulupirika
koma amalanga kwathunthu anthu odzikuza.
24 Khalani ndi nyonga ndipo limbani mtima,
inu nonse amene mumayembekezera Yehova.

## Salimo 32

Salimo la Davide. Malangizo.

1 Ngodala munthu
amene zolakwa zake zakhululukidwa;
amene machimo ake aphimbidwa.
2 Ngodala munthu
amene machimo ake Yehova sawawerengeranso pa iye
ndipo mu mzimu mwake mulibe chinyengo.

3 Pamene ndinali chete,
mafupa anga anakalamba
chifukwa cha kubuwula kwanga tsiku lonse.
4 Pakuti usana ndi usiku
dzanja lanu linandipsinja;
mphamvu zanga zinatha
monga nthawi yotentha yachilimwe.
Sela
5 Kotero ine ndinavomereza tchimo langa kwa Inu,
sindinabise mphulupulu zanga.
Ndinati, "Ine ndidzawulula
zolakwa zanga kwa Yehova,
ndipo Inu munandikhululukira
mlandu wa machimo anga."
Sela

6 Choncho aliyense okhulupirika apemphere kwa Inuyo
pomwe mukupezeka;
ndithu pamene madzi amphamvu auka,
sadzamupeza.
7 Inu ndi malo anga obisala;
muzinditeteza ku mavuto ndipo muzindizinga
ndi nyimbo zachipulumutso.
Sela

8 Ndidzakulangiza ndi kukuphunzitsa njira imene udzayendamo;
ndidzakupatsa uphungu ndi kukuyang'anira.
9 Usakhale ngati kavalo kapena bulu,
zimene zilibe nzeru,
koma ziyenera kuwongoleredwa ndi zitsulo za m'kamwa ndi pamutu,
ukapanda kutero sizibwera kwa iwe.
10 Zowawa ndi zambiri za anthu oyipa
koma chikondi chosatha cha Yehova
chimamuzinga munthu amene amadalira Iye.

11 Kondwerani mwa Yehova inu olungama;
imbani, inu nonse amene muli owongoka mtima!

# Salimo 33

1 Imbirani Yehova mokondwera Inu olungama,
n'koyenera kuti owongoka mtima azitamanda Iyeyo.
2 Mutamandeni Yehova ndi pangwe;
muyimbireni Iye nyimbo pa zeze wa zingwe khumi.
3 Muyimbireni nyimbo yatsopano;
imbani mwaluso, ndipo fuwulani mwachimwemwe.

4 Pakuti mawu a Yehova ndi olungama ndi owona;
Iye ndi wokhulupirika pa zonse zimene amachita.
5 Yehova amakonda chilungamo ndipo amaweruza molungama;
dziko lapansi ladzaza ndi chikondi chake chosatha.

6 Ndi mawu a Yehova mayiko akumwamba anapangidwa,
zolengedwa zake ndi mpweya wa m'kamwa mwake.
7 Iye amasonkhanitsa pamodzi madzi a m'nyanja m'mitsuko;
amayika zozama m'nyumba zosungiramo.
8 Dziko lonse lapansi liope Yehova;
anthu onse amulemekeze Iye.
9 Pakuti Iye anayankhula ndipo zinakhalapo;
Iye analamulira ndipo zinakhazikika.
10 Yehova amalepheretsa chikonzero cha anthu a mitundu ina;
Iye amaphwanya zolinga za anthu ambiri.
11 Koma chikonzero cha Yehova chimakhala mpaka muyaya,
zolinga za mu mtima mwake pa mibado yonse.

12 Wodala mtundu wa anthu umene Mulungu wake ndi Yehova,
anthu amene Iye anawasankha kukhala cholowa chake.
13 Kuchokera kumwamba Yehova amayang'ana pansi
ndi kuona anthu onse;
14 kuchokera ku malo ake okhalako Iye amayang'anira
onse amene amakhala pa dziko lapansi.
15 Iye amene amapanga mitima ya onse,
amaona zonse zimene akuchita.
16 Palibe mfumu imene imapulumutsidwa chifukwa cha kukula kwa gulu
lake lankhondo;
palibe msilikali amene amathawa ndi mphamvu zake zazikulu.
17 Kavalo ndi chiyembekezo cha chabechabe cha chipulumutso,
ngakhale ali ndi mphamvu yayikulu sangathe kupulumutsa.
18 Koma maso a Yehova ali pa iwo amene amaopa Iye;
amene chiyembekezo chawo chili m'chikondi chake chosatha,
19 kuwawombola iwo ku imfa
ndi kuwasunga ndi moyo nthawi ya njala.

20 Ife timadikira kwa Yehova mwachiyembekezo;
Iye ndiye thandizo lathu ndi chishango chathu.
21 Mwa Iye mitima yathu imakondwera,
pakuti ife timadalira dzina lake loyera.
22 Chikondi chanu chosatha
chikhale pa ife Inu Yehova, pamene tikuyembekeza kwa Inu.

# Salimo 34

Salimo la Davide. Pamene iye ananyengezera misala pamaso pa Abimeleki, amene anamupirikitsa, iyeyo n'kuchoka.
1 Ndidzayamika Yehova nthawi zonse;
matamando ake adzakhala pa milomo yanga nthawi zonse.
2 Moyo wanga udzanyadira Yehova;
anthu osautsidwa amve ndi kukondwera.
3 Lemekezani Yehova pamodzi ndi ine;
tiyeni pamodzi tikuze dzina lake.

4 Ine ndinafunafuna Yehova ndipo Iye anandiyankha;
anandilanditsa ku mantha anga onse.
5 Iwo amene amayang'ana kwa Iye, nkhope zawo zimanyezimira;
nkhope zawo sizikhala zophimbidwa ndi manyazi.
6 Munthu wosauka uno anayitana, ndipo Yehova anamumva;
Yehova anamupulumutsa ku mavuto ake onse.
7 Mngelo wa Yehova amatchinjiriza amene amakonda Iye
ndi kuwalanditsa.

8 Lawani ndipo onani kuti Yehova ndi wabwino;
wodala munthu amene amathawira kwa Iye.
9 Wopani Yehova inu oyera mtima ake,
pakuti iwo amene amaopa Iye sasowa kanthu.
10 Mikango itha kulefuka ndi kumva njala
koma iwo amene amafunafuna Yehova sasowa kanthu kalikonse kabwino.

11 Bwerani ana anga, mundimvere;
ndidzakuphunzitsani kuopa Yehova.
12 Aliyense wa inu amene amakonda moyo wake
ndi kukhumba kuti aone masiku abwino ambiri,
13 asunge lilime lake ku zoyipa
ndi milomo yake kuti isayankhule zonama.
14 Tembenuka kuchoka ku zoyipa ndipo chita zabwino;
funafuna mtendere ndi kuwulondola.

15 Maso a Yehova ali pa olungama
ndipo makutu ake ali tcheru kumva kulira kwawo;
16 nkhope ya Yehova ikutsutsana ndi amene amachita zoyipa,
kuwachotsa kuti asawakumbukirenso pa dziko lapansi.

17 Olungama amafuwula, ndipo Yehova amawamva;
Iye amawalanditsa ku mavuto awo onse.
18 Yehova ali pafupi kwa osweka mtima
ndipo amapulumutsa iwo amene asweka mu mzimu.

19 Munthu wolungama atha kukhala ndi mavuto ambiri,
Koma Yehova amamulanditsa ku mavuto onsewo,
20 Iye amateteza mafupa ake onse,
palibe limodzi la mafupawo limene lidzathyoledwa.

21 Choyipa chidzapha anthu oyipa;
adani a olungama adzapezeka olakwa.
22 Yehova amawombola atumiki ake;
aliyense amene amathawira kwa Iye sadzapezeka wolakwa.

# Salimo 35

Salimo la Davide.
1 Inu Yehova, mulimbane nawo amene akulimbana nane;
mumenyane nawo amene akumenyana nane.
2 Tengani chishango ndi lihawo;
dzukani ndipo bwerani mundithandize.

3 Tengani mkondo ndi nthungo,
kulimbana ndi iwo amene akundithamangitsa.
Uzani moyo wanga kuti,
"Ine ndine chipulumutso chako."

4 Iwo amene akufunafuna moyo wanga
anyozedwe ndi kuchita manyazi;
iwo amene akukonza kuti moyo wanga uwonongeke
abwerere m'mbuyo mochititsa mantha.
5 Akhale ngati mankhusu owuluka ndi mphepo
pamene mngelo wa Yehova akuwapirikitsa.
6 Njira yawo ikhale ya mdima ndi yoterera
pamene mngelo wa Yehova akuwathamangitsa.
7 Popeza ananditchera ukonde popanda chifukwa
ndipo popanda chifukwa andikumbira dzenje,
8 chiwonongeko chiwapeza modzidzimutsa
ukonde umene iwo abisa uwakole,
agwere m'dzenje kuti awonongedwe.
9 Pamenepo moyo wanga udzakondwera mwa Yehova
ndi kusangalala ndi chipulumutso chake.
10 Thupi langa lidzafuwula mokondwera,
"Ndani angafanane nanu Yehova?
Mumalanditsa osauka kwa amene ali ndi mphamvu zambiri,
osauka ndi osowa kwa iwo amene amawalanda."

11 Mboni zopanda chisoni zinayimirira,
zinandifunsa zinthu zimene sindikuzidziwa.
12 Iwo anandibwezera zoyipa pa zabwino
ndipo anasiya moyo wanga pa chisoni.
13 Koma pamene iwo ankadwala, ine ndinavala chiguduli
ndi kudzichepetsa ndekha posala zakudya.
Pamene mapemphero anga anabwerera kwa ine osayankhidwa,
14 ndinayendayenda ndi kulira maliro,
kumulira ngati bwenzi langa kapena m'bale wanga.
Ndinaweramitsa mutu wanga mosweka mtima
kukhala ngati ndikulira amayi anga.
15 Koma pamene ndinaphunthwa, iwo anasonkhana mosangalala;
ondithira nkhondo anasonkhana kutsutsana nane, ineyo osadziwa.
Iwo sanasiye kundiyankhulira mawu onyoza.
16 Monga anthu osapembedza, iwo anandinyoza mwachipongwe;
anandikukutira mano awo.
17 Ambuye, mpaka liti mudzakhala mukungoyang'ana?
Landitsani moyo wanga ku chiwonongeko chawo,
moyo wanga wopambana ku mikango.
18 Ndidzakuyamikani mu msonkhano waukulu;
pakati pa gulu lalikulu la anthu ndidzakutamandani.

19 Musalole adani anga onyenga
akondwere chifukwa cha masautso anga;
musalole kuti amene amadana nane popanda chifukwa
andiyang'ane cham'mbali mondinyoza.
20 Iwowo sayankhula mwamtendere,

koma amaganizira zonamizira
iwo amene amakhala mwabata m'dziko.
21 Iwo amandiseka mofuwula ndipo amati, "Haa! Haa!
Ndipo ndi maso athuwa ife taziona."

22 Yehova mwaona zimenezi; musakhale chete.
Ambuye musakhale kutali ndi ine.
23 Dzukani, ndipo nyamukani kunditeteza!
Mulimbane nawo chifukwa cha ine, Mulungu wanga ndi Ambuye anga.
24 Onetsani kusalakwa kwanga mwa chilungamo chanu, Inu Yehova Mulungu wanga.
Musalole kuti akondwere chifukwa cha mavuto anga.
25 Musalole kuti aganize kuti, "Amati atani, zachitika monga momwe timafunira!"
Kapena kunena kuti, "Tamutha ameneyu basi."

26 Onse amene amakondwera ndi masautso anga
achite manyazi ndi kusokonezeka.
Onse amene amadzikweza kufuna kundipambana,
avekedwe manyazi ndi mnyozo ngati zovala.
27 Koma amene amakondwera chifukwa chakuti ndine wosalakwa,
afuwule mwachimwemwe ndi chisangalalo.
Nthawi zonse azinena kuti, "Yehova akwezeke,
Iye amene amakondwera ndi kupeza bwino kwa mtumiki wake."
28 Pakamwa panga padzayankhula za chilungamo chanu
ndi za matamando anu tsiku lonse.

# Salimo 36

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide, mtumiki wa Yehova.
1 Uthenga uli mu mtima mwanga
wonena za kuchimwa kwa munthu woyipa:
Mu mtima mwake
mulibe kuopa Mulungu.
2 Pakuti iye m'kuona kwake amadzinyenga yekha kwambiri,
sazindikira kapena kudana ndi tchimo lake.
3 Mawu a pakamwa pake ndi oyipa ndi achinyengo;
iyeyo waleka kukhala wanzeru ndi kuchita zabwino.
4 Ngakhale ali pa bedi pake amakonzekera zoyipa;
iye amadzipereka yekha ku njira ya uchimo
ndipo sakana cholakwa chilichonse.

5 Chikondi chanu Yehova, chimafika ku mayiko a kumwamba,
kukhulupirika kwanu mpaka ku mitambo.
6 Chilungamo chanu Mulungu chili ngati mapiri aakulu,
chiweruzo chanu chili ngati kuzama kwakukulu.
Yehova mumasunga munthu pamodzi ndi chinyama.
7 Chikondi chanu chosatha ndi chamtengowapatali!
Otchuka pamodzi ndi anthu wamba pakati pa anthu
amapeza pothawirapo mu mthunzi wa mapiko anu.
8 Iwo amadyerera zinthu zambiri za m'nyumba yanu;

Inu mumawapatsa chakumwa kuchokera mu mtsinje wanu wachikondwerero.
9 Pakuti kwa Inu kuli kasupe wamoyo;
m'kuwala kwanu ifenso timaona kuwala.

10 Pitirizani chikondi chanu pa iwo amene amakudziwani,
chilungamo chanu kwa olungama mtima.
11 Musalole kuti phazi la wodzikuza libwere kulimbana nane,
kapena dzanja la oyipa kundithamangitsa.
12 Onani momwe ochita zoyipa agonera atagwa,
aponyeni pansi, kuti asathe kudzukanso!

# Salimo 37

Salimo la Davide.
1 Usamavutike chifukwa cha anthu oyipa
kapena kuchitira nsanje amene akuchita cholakwa;
2 pakuti monga udzu iwo adzafota msanga,
ngati mbewu zobiriwira adzanyala msanga.

3 Khulupirira Yehova ndipo uzichita zabwino;
khazikika m'dziko ndi kutsata zokhulupirika.
4 Udzikondweretse wekha mwa Yehova
ndipo Iye adzakupatsa zokhumba za mtima wako.

5 Pereka njira yako kwa Yehova;
dalira Iye ndipo Iyeyo adzachita izi:
6 Iye adzachititsa chilungamo chako kuwala ngati m'bandakucha,
chiweruzo chako ngati dzuwa la masana.

7 Khala chete pamaso pa Yehova ndipo umudikire mofatsa;
usavutike pamene anthu apambana m'njira zawo,
pamene iwo achita zinthu zawo zoyipa.

8 Pewa kupsa mtima ndipo tembenuka kuchoka ku ukali,
usavutike chifukwa zimenezi zimatsogolera ku zoyipa.
9 Pakuti anthu oyipa adzachotsedwa,
koma iwo amene amayembekeza mwa Yehova adzalandira dziko.

10 Kwa kanthawi oyipa sadzapezekanso;
ngakhale muwafunefune, sadzapezekanso.
11 Koma ofatsa adzalandira dziko
ndipo adzasangalala ndi mtendere waukulu.

12 Oyipa amakonza chiwembu kutsutsana ndi olungama
ndipo amawakukutira mano;
13 koma Ambuye amaseka oyipa
pakuti Iye amadziwa kuti tsiku lawo likubwera.

14 Oyipa amasolola lupanga
ndi kupinda uta
kugwetsa osauka ndi osowa,
kupha iwo amene njira zawo ndi zolungama.

15 Koma malupanga awo analasa mitima yawo yomwe,
ndipo mauta awo anathyoka.

16 Zabwino zochepa zimene olungama ali nazo
ziposa chuma cha anthu oyipa ambiri;
17 pakuti mphamvu ya oyipa idzasweka,
koma Yehova amasunga olungama.

18 Masiku a anthu osalakwa amadziwika ndi Yehova,
ndipo cholowa chawo chidzakhala mpaka muyaya.
19 Pa nthawi ya mavuto iwo sadzafota;
m'masiku a njala adzakhala ndi zinthu zambiri.

20 Koma oyipa adzawonongeka;
adani a Yehova adzakhala ngati kukongola kwa kuthengo,
iwo adzazimirira ngati utsi.

21 Oyipa amabwereka ndipo sabweza
koma olungama amapereka mowolowamanja.
22 Iwo amene Yehova amawadalitsa adzalandira dziko,
koma amene Iye amawatemberera adzachotsedwa.

23 Ngati Yehova akondwera ndi njira ya munthu,
amakhazikitsa mayendedwe ake;
24 ngakhale atapunthwa sadzagwa,
pakuti Yehova amamutchinjiriza ndi dzanja lake.

25 Ine ndinali wamng'ono ndipo tsopano ndakalamba
koma sindinaonepo olungama akusiyidwa
kapena ana awo akupempha chakudya.
26 Iwo ndi owolowamanja nthawi zonse ndipo amabwereketsa mwaufulu;
ana awo adzadalitsika.

27 Tembenuka kuchoka ku zoyipa ndipo chita zabwino;
pamenepo udzakhazikika m'dziko kwamuyaya.
28 Pakuti Yehova amakonda wolungama
ndipo sadzasiya okhulupirika ake.

Iwo adzatetezedwa kwamuyaya,
koma zidzukulu za oyipa zidzachotsedwa;
29 olungama adzalandira dziko
ndipo adzakhazikikamo kwamuyaya.

30 Pakamwa pa munthu wolungama pamayankhula za nzeru,
ndipo lilime lake limayankhula zolungama.
31 Lamulo la Mulungu wake lili mu mtima mwake;
mapazi ake saterereka.

32 Oyipa amabisala kudikira olungama;
kufunafuna miyoyo yawoyo;
33 koma Yehova sadzawasiya pansi pa mphamvu yawo
kapena kuti atsutsidwe pamene abweretsedwa pa milandu.

34 Khulupirira Yehova,
ndipo sunga njira yake;
Iye adzakukweza ndipo udzalandira dziko kuti likhale lako;
udzaona anthu oyipa akuwonongeka.

35 Ine ndinaona munthu woyipa ndi munthu wopanda chifundo
akupeza bwino ngati mtengo wobiriwira pa nthaka ya makolo ake.
36 Koma sanachedwe kumwalira ndipo sanaonekenso;
ngakhale ndinamuyang'anayang'ana, sanapezekenso.

37 Ganizira za munthu wosalakwa, yang'anitsitsa munthu wolungama;
udzaona kuti ali ndi tsogolo labwino ndipo ali ndi zidzukulu zambiri.
38 Koma anthu ochimwa adzawonongeka;
iwowo pamodzi ndi zidzukulu zawo zomwe.

39 Chipulumutso cha olungama chimachokera kwa Yehova;
Iye ndiye linga lawo pa nthawi ya masautso.
40 Yehova amawathandiza ndi kuwalanditsa;
Iye amawalanditsa kwa oyipa ndi kuwapulumutsa,
pakuti amathawira kwa Iye.

# Salimo 38

Salimo la Davide. Kupempha.

1 Yehova musandidzudzule mutapsa mtima
kapena kundilanga muli ndi ukali.
2 Pakuti mivi yanu yandilasa,
ndipo dzanja lanu latsika ndipo landifikira.
3 Chifukwa cha ukali wanu mulibe thanzi m'thupi langa;
mafupa anga alibe mphamvu chifukwa cha tchimo langa.
4 Kulakwa kwanga kwandipsinja
ngati katundu wolemera kwambiri kuposa mphamvu zanga.

5 Mabala anga akuwola ndipo akununkha
chifukwa cha uchitsiru wa moyo wanga wauchimo.
6 Ine ndapindika msana ndipo ndawerama kwambiri;
tsiku lonse ndimangolira.
7 Msana wanga wagwidwa ndi ululu wosasimbika,
mulibe thanzi m'thupi langa.
8 Ndilibe mphamvu ndipo ndakunthidwa kwathunthu;
ndikubuwula ndi ululu wa mumtima.

9 Zokhumba zanga zonse zili poonekera pamaso panu Ambuye,
kusisima kwanga sikunabisike kwa Inu.
10 Mtima wanga ukugunda, mphamvu zanga zikutha;
ngakhale kuwala kwachoka m'maso mwanga.
11 Abwenzi anga ndi anzanga akundipewa chifukwa cha mabala anga;
anansi anga akhala kutali nane.
12 Iwo amene akufunafuna moyo wanga atchera misampha yawo,
oti andipwetekewo amayankhula za kuwonongeka kwanga;
tsiku lonse amakonza zachinyengo.

13 Ine ndili ngati munthu wosamva amene sangamve,
monga wosayankhula, amene sangathe kutsekula pakamwa pake;
14 Ndakhala ngati munthu amene samva,
amene pakamwa pake sipangathe kuyankha.
15 Ndikudikira Inu Yehova;
mudzayankha, Inu Ambuye Mulungu wanga.
16 Pakuti Ine ndinati, "Musawalole kuti akondwere
kapena kudzikweza okha pa ine pamene phazi langa laterereka."

17 Pakuti ndili pafupi kugwa,
ndipo ndikumva kuwawa nthawi zonse.
18 Ndikuvomereza mphulupulu zanga;
ndipo ndavutika ndi tchimo langa.
19 Ambiri ndi adani anga amphamvu;
amene amandida popanda chifukwa alipo ochuluka kwambiri.
20 Iwo amene amandibwezera zoyipa m'malo mwa zabwino
amandinyoza pamene nditsatira zabwino.

21 Inu Yehova, musanditaye;
musakhale kutali ndi ine Mulungu wanga.
22 Bwerani msanga kudzandithandiza,
Inu Ambuye Mpulumutsi wanga.

# Salimo 39

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Kwa Yedutuni. Salimo la Davide.
1 Ndinati, "Ndidzasamalira njira zanga
ndipo ndidzasunga lilime langa kuti ndisachimwe;
ndidzatseka pakamwa panga ndi chitsekerero
nthawi yonse imene woyipa ali pamaso panga."
2 Koma pamene ndinali chete
osanena ngakhale kanthu kalikonse kabwino
mavuto anga anachulukirabe.
3 Mtima wanga unatentha m'kati mwanga,
ndipo pamene ndinkalingalira, moto unayaka;
kenaka ndinayankhula ndi lilime langa:

4 "Yehova ndionetseni mathero a moyo wanga
ndi chiwerengero cha masiku anga;
mundidziwitse kuti moyo wanga ndi wosakhalitsa motani.
5 Inu mwachititsa kuti masiku anga akhale ochepa kwambiri,
kutalika kwa zaka zanga ndi kopanda phindu pamaso panu;
moyo wa munthu aliyense ndi waufupi.
Sela
6 Munthu ali ngati chithunzithunzi chake pamene akuyenda uku ndi uku:
Iye amangovutika koma popanda phindu;
amadzikundikira chuma, osadziwa kuti chidzakhala chayani.

7 "Koma tsopano Ambuye kodi ndifunanso chiyani?
Chiyembekezo changa chili mwa Inu.
8 Pulumutseni ku zolakwa zanga zonse;
musandisandutse chonyozeka kwa opusa.
9 Ine ndinali chete; sindinatsekule pakamwa panga

pakuti Inu ndinu amene mwachita zimenezi.
10 Chotsani mkwapulo wanu pa ine;
ndagonjetsedwa ndi nkhonya ya dzanja lanu.
11 Inu mumadzudzula ndi kulanga anthu chifukwa cha tchimo lawo;
mumawononga chuma chawo monga njenjete;
munthu aliyense ali ngati mpweya.
Sela

12 "Imvani pemphero langa Inu Yehova,
mverani kulira kwanga kopempha thandizo;
musakhale chete pamene ndikulirira kwa Inu,
popeza ndine mlendo wanu wosakhalitsa;
monga anachitira makolo anga onse.
13 Musandiyang'ane mwaukali, choncho ndidzatha kusangalala
ndisanafe ndi kuyiwalika."

# Salimo 40

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Mofatsa ndinadikira Yehova
Iye anatembenukira kwa ine ndipo anamva kulira kwanga.
2 Ananditulutsa m'dzenje lachitayiko,
m'thope ndi m'chithaphwi;
Iye anakhazikitsa mapazi anga pa thanthwe
ndipo anandipatsa malo oyimapo olimba.
3 Iye anayika nyimbo yatsopano m'kamwa mwanga,
nyimbo yamatamando kwa Mulungu wanga.
Ambiri adzaona,
nadzaopa ndipo adzakhulupirira Yehova.

4 Ndi wodala munthu
amakhulupirira Yehova;
amene sayembekezera kwa odzikuza,
kapena kwa amene amatembenukira kwa milungu yabodza.
5 Zambiri, Yehova Mulungu wanga,
ndi zodabwitsa zimene Inu mwachita.
Zinthu zimene munazikonzera ife
palibe amene angathe kukuwerengerani.
Nditati ndiyankhule ndi kufotokozera,
zidzakhala zambiri kuzifotokoza.

6 Nsembe ndi zopereka Inu simuzifuna,
koma makutu anga mwawatsekula;
zopereka zopsereza ndi zopereka chifukwa cha tchimo
Inu simunazipemphe.
7 Kotero ndinati, "Ndili pano, ndabwera.
M'buku mwalembedwa za ine.
8 Ndikufuna kuchita chifuniro chanu, Inu Mulungu wanga;
lamulo lanu lili mu mtima mwanga."

9 Ndikulalikira uthenga wa chilungamo chanu mu msonkhano waukulu;
sinditseka milomo yanga
monga mukudziwa Inu Yehova.

10 Sindibisa chilungamo chanu mu mtima mwanga;
ndinayankhula za kukhulupirika kwanu ndi chipulumutso chanu.
Ine sindiphimba chikondi chanu ndi choonadi chanu
pa msonkhano waukulu.

11 Musandichotsere chifundo chanu Yehova;
chikondi chanu ndi choonadi chanu zinditeteze nthawi zonse.
12 Pakuti mavuto osawerengeka andizungulira;
machimo anga andigonjetsa, ndipo sindingathe kuona.
Alipo ambiri kuposa tsitsi la m'mutu mwanga,
ndipo mtima wanga ukufowoka m'kati mwanga.

13 Pulumutseni Yehova;
Bwerani msanga Yehova kudzandithandiza.
14 Onse amene akufunafuna kuchotsa moyo wanga
achititsidwe manyazi ndi kusokonezedwa;
onse amene amakhumba chiwonongeko changa
abwezedwe mwamanyazi.
15 Iwo amene amanena kwa ine kuti, "Hee! Hee!"
abwerere akuchita manyazi.
16 Koma iwo amene amafunafuna Inu
akondwere ndi kusangalala mwa Inu;
iwo amene amakonda chipulumutso chanu
nthawi zonse anene kuti, "Yehova akwezeke!"

17 Komabe Ine ndine wosauka ndi wosowa;
Ambuye andiganizire.
Inu ndinu thandizo langa ndi wondiwombola wanga;
Inu Mulungu wanga, musachedwe.

# Salimo 41

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Wodala ndi munthu amene amaganizira anthu osauka;
Yehova amamuwombola pa nthawi yamsautso.
2 Yehova adzamuteteza ndi kusunga moyo wake;
Yehova adzamudalitsa iye m'dziko
ndipo sadzamupereka ku zofuna za adani ake.
3 Yehova adzamuthandiza pamene akudwala
ndipo adzamuchiritsa pa bedi lake la matenda.

4 Ndinati, "Inu Yehova, mundichitire chifundo;
chiritseni pakuti ndakuchimwirani."
5 Adani anga mwankhwidzi amanena za ine kuti,
"Kodi munthu ameneyu adzafa liti kuti ayiwalike?"
6 Pamene wina abwera kudzandiona,
amayankhula mwachinyengo, pomwe mtima wake ukusonkhanitsa zachipongwe;
kenaka iye amatuluka ndi kukalengeza kunja.

7 Adani anga onse amanong'onezana pamodzi kulimbana nane,
iwo amalingalira zoyipa kwambiri za ine, ponena kuti,
8 "Matenda owopsa amugwira;

sadzaukapo pamalo pamene wagona."
9 Ngakhale bwenzi langa la pamtima amene ndinamudalira,
iye amene amadya pamodzi ndi ine
watukula chidendene chake kulimbana nane.

10 Koma Yehova mundichititire chifundo,
dzutseni kuti ndiwabwezere.
11 Ine ndikudziwa kuti mukukondwera nane,
pakuti mdani wanga sandigonjetsa.
12 Mu ungwiro wanga Inu mumandisunga
ndi kundiyimika pamaso panu kwamuyaya.

13 Atamandike Yehova Mulungu wa Israeli
kuchokera muyaya mpaka muyaya.
Ameni ndi Ameni.

# BUKU LACHIWIRI

## 42

*Masalimo 42–72*

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Ndakatulo ya ana a Kora.
1 Monga mbawala ipuma wefuwefu kufunafuna mitsinje yamadzi,
kotero moyo wanga upuma wefuwefu kufunafuna Inu Mulungu.
2 Moyo wanga uli ndi ludzu lofuna Mulungu, lofuna Mulungu wamoyo.
Kodi ndipite liti kukakumana ndi Mulungu?
3 Misozi yanga yakhala chakudya changa
usana ndi usiku,
pamene anthu akunena kwa ine tsiku lonse kuti,
"Mulungu wako ali kuti?"
4 Zinthu izi ndimazikumbukira
pamene ndikukhuthula moyo wanga:
momwe ndinkapitira ndi gulu lalikulu,
kutsogolera mayendedwe a ku Nyumba ya Mulungu
ndi mfuwu yachimwemwe ndi mayamiko
pakati pa anthu a pa chikondwerero.

5 N'chifukwa chiyani uli ndi chisoni, iwe moyo wanga?
N'chifukwa chiyani wakhumudwa iwe m'kati mwanga?
Yembekezera Mulungu,
pakuti ndidzamulambirabe,
Mpulumutsi wanga ndi 6 Mulungu wanga.

Moyo wanga uli ndi chisoni m'kati mwanga
kotero ndidzakumbukira Inu
kuchokera ku dziko la Yorodani,
ku mitunda ya Herimoni kuchokera ku phiri la Mizara.
7 Madzi akuya akuyitana madzi akuya
mu mkokomo wa mathithi anu;
mafunde anu onse obwera mwamphamvu
andimiza.

8 Koma usana Yehova amalamulira chikondi chake,
nthawi ya usiku nyimbo yake ili nane;
pemphero kwa Mulungu wa moyo wanga.

9 Ine ndikuti kwa Mulungu Thanthwe langa,
“N’chifukwa chiyani mwandiyiwala?
N’chifukwa chiyani ndiyenera kuyenda ndikulira,
woponderezedwa ndi mdani?”
10 Mafupa anga ali ndi ululu wakufa nawo
pamene adani anga akundinyoza,
tsiku lonse akunena kuti,
“Mulungu wako ali kuti?”

11 Bwanji ukumva chisoni,
iwe mtima wanga?
Chifukwa chiyani ukuvutika chonchi m’kati mwanga?
Khulupirira Mulungu, pakuti ndidzamutamandanso,
Iye amene ali thandizo langa ndi Mulungu wanga.

# Salimo 43

1 Onetsani kusalakwa kwanga Inu Mulungu;
ndipo mundinenere mlandu wanga kutsutsana ndi mtundu wosapembedza;
mundilanditse m’manja mwa achinyengo ndi anthu oyipa.
2 Pajatu Inu Mulungu ndinu mphamvu zanga.
N’chifukwa chiyani mwandikana ine?
N’chifukwa chiyani ndiyenera kuyenda ndikulira,
woponderezedwa ndi mdani?
3 Tumizani kuwunika kwanu ndi choonadi chanu
kuti zinditsogolere;
mulole kuti zindifikitse ku phiri lanu loyera,
kumalo kumene inu mumakhala.
4 Ndipo ndidzapita ku guwa lansembe la Mulungu,
kwa Mulungu, chimwemwe changa ndi chikondwerero changa.
Ndidzakutamandani ndi zeze,
Inu Mulungu wanga.

5 N’chifukwa chiyani uli ndi chisoni iwe moyo wanga?
N’chifukwa chiyani wakhumudwa iwe m’kati mwanga?
Khulupirira Mulungu,
pakuti ndidzamutamandabe Iye,
Mpulumutsi wanga ndi Mulungu wanga.

# Salimo 44

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Ndakatulo ya ana a Kora.
1 Ife tamva ndi makutu athu, Inu Mulungu;
makolo athu atiwuza
zimene munachita m’masiku awo,
masiku akalekalewo.
2 Ndi dzanja lanu munathamangitsa mitundu ya anthu ena
ndi kudzala makolo athu;
Inu munakantha mitundu ya anthu,
koma makolo athuwo Inu munawapatsa ufulu.
3 Sanalande dziko ndi lupanga lawo,
si mkono wawo umene unawabweretsera chigonjetso,

koma ndi dzanja lanu lamanja, mkono wanu ndi kuwala kwa nkhope yanu,
pakuti munawakonda.

4 Inu ndinu Mfumu yanga ndi Mulungu wanga
amene mumalamulira chigonjetso cha Yakobo.
5 Kudzera kwa inu ife timabweza adani athu;
kudzera m'dzina lanu timapondereza otiwukirawo.
6 Sindidalira uta wanga,
lupanga langa silindibweretsera chigonjetso;
7 koma Inu mumatigonjetsera adani athu,
mumachititsa manyazi amene amadana nafe.
8 Timanyadira mwa Mulungu wathu tsiku lonse,
ndipo tidzatamanda dzina lanu kwamuyaya.

9 Koma tsopano mwatikana ndi kutichepetsa;
Inu simupitanso ndi ankhondo athu.
10 Munachititsa ife kubwerera m'mbuyo pamaso pa mdani
ndipo amene amadana nafe atilanda katundu.
11 Inu munatipereka kuti tiwonongedwe monga nkhosa
ndipo mwatibalalitsa pakati pa anthu a mitundu ina.
12 Inu munagulitsa anthu anu pa mtengo wotsika,
osapindulapo kanthu pa malondawo.

13 Mwachititsa kuti tikhale chochititsa manyazi kwa anthu a mitundu ina,
chonyozeka ndi chothetsa nzeru kwa iwo amene atizungulira.
14 Mwachititsa kuti tikhale onyozeka pakati pa anthu a mitundu ina;
anthu amapukusa mitu yawo akationa.
15 Manyazi anga ali pamaso panga tsiku lonse
ndipo nkhope yanga yaphimbidwa ndi manyazi
16 chifukwa cha mawu otonza a iwo amene amandinyoza ndi kundichita chipongwe,
chifukwa cha mdani amene watsimikiza kubwezera.

17 Zonsezi zinatichitikira
ngakhale kuti ifeyo sitinayiwale Inu
kapena kuonetsa kusakhulupirika pa pangano lanu.
18 Mitima yathu sinabwerere m'mbuyo;
mapazi athu sanatayike pa njira yanu.
19 Koma Inu mwatiphwanya ndi kuchititsa kuti tikhale ozunzidwa ndi ankhandwe
ndipo mwatiphimba ndi mdima waukulu.

20 Tikanayiwala dzina la Mulungu wathu
kapena kutambasulira manja athu kwa mulungu wachilendo,
21 kodi Mulungu wathu sakanazidziwa zimenezi,
pakuti Iye amadziwa zinsinsi zamumtima?
22 Komabe chifukwa cha Inu timakumana ndi imfa tsiku lonse,
tili ngati nkhosa zoyenera kuti ziphedwe.

23 Dzukani Ambuye! N'chifukwa chiyani mukugona!

Dziwutseni nokha! Musatikane kwamuyaya.
24 N'chifukwa chiyani mukubisa nkhope yanu,
ndi kuyiwala mavuto athu ndi kuponderezedwa kwathu?

25 Tatsitsidwa pansi mpaka pa fumbi;
matupi athu amatirira pa dothi.
26 Imirirani ndi kutithandiza,
tiwomboleni chifukwa cha chikondi chanu chosasinthika.

# Salimo 45

Kwa mtsogoleri wamayimbidwe. Monga mwa mayimbidwe a "Maluwa a Kakombo." Salimo la ana a Kora. Nyimbo ya pa ukwati.

1 Mtima wanga watakasika ndi nkhani yokoma
pamene ndikulakatula mawu anga kwa mfumu;
lilime langa ndi cholembera cha wolemba waluso.

2 Inu ndinu abwino kwambiri kuposa anthu onse
ndipo milomo yanu inadzozedwa ndi chikondi cha Mulungu chosasinthika,
popeza Mulungu wakudalitsani kwamuyaya.
3 Mangirirani lupanga lanu m'chiwuno mwanu, inu munthu wamphamvu;
mudziveke nokha ndi ulemerero ndi ukulu wanu.
4 Mu ukulu wanu mupite mutakwera mwachigonjetso
m'malo mwa choonadi, kudzichepetsa ndi chilungamo;
dzanja lanu lamanja lionetsere ntchito zanu zoopsa.
5 Mivi yanu yakuthwa ilase mitima ya adani a mfumu,
mitundu ya anthu igwe pansi pa mapazi anu.
6 Mpando wanu waufumu, Inu Mulungu, udzakhala ku nthawi za nthawi;
ndodo yaufumu yachilungamo idzakhala ndodo yaufumu ya ufumu wanu.
7 Inu mumakonda chilungamo ndi kudana ndi zoyipa;
choncho Mulungu, Mulungu wanu, wakukhazikani pamwamba pa anzanu
pokudzozani ndi mafuta a chimwemwe.
8 Mikanjo yanu yonse ndi yonunkhira ndi mure ndi aloe ndi kasiya;
kuchokera ku nyumba zaufumu zokongoletsedwa ndi mnyanga wanjovu
nyimbo za zoyimbira zazingwe zimakusangalatsani.
9 Ana aakazi a mafumu ali pakati pa akazi anu olemekezeka;
ku dzanja lanu lamanja kuli mkwatibwi waufumu ali mu golide wa ku Ofiri.

10 Tamvera, iwe mwana wa mkazi ganizira ndipo tchera khutu;
iwala anthu ako ndi nyumba ya abambo ako.
11 Mfumu yathedwa nzeru chifukwa cha kukongola kwako;
mulemekeze pakuti iyeyo ndiye mbuye wako.
12 Mwana wa mkazi wa ku Turo adzabwera ndi mphatso,
amuna a chuma adzafunafuna kukoma mtima kwako.

13 Wokongola kwambiri ndi mwana wa mfumu ali m'chipinda mwake,
chovala chake ndi cholukidwa ndi thonje ndi golide.
14 Atavala zovala zamaluwamaluwa akupita naye kwa mfumu;

anamwali okhala naye akumutsatira
ndipo abweretsedwa kwa inu.
15 Iwo akuwaperekeza ndi chimwemwe ndi chisangalalo;
akulowa m'nyumba yaufumu.

16 Ana ako aamuna adzatenga malo a makolo ako;
udzachititsa kuti akhale ana a mfumu m'dziko lonse.
17 Ndidzabukitsa mbiri yako m'mibado yonse;
choncho mitundu yonse idzakutamanda ku nthawi za nthawi.

# Salimo 46

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Ndakatulo ya ana a Kora. Nyimbo ya anamwali.
1 Mulungu ndiye kothawira kwathu ndi mphamvu yathu,
thandizo lopezekeratu pa nthawi ya mavuto.
2 N'chifukwa chake sitidzaopa ngakhale dziko lapansi lisunthike,
ngakhale mapiri agwe pakati pa nyanja,
3 ngakhale madzi ake atakokoma ndi kuchita thovu,
ngakhale mapiri agwedezeke ndi kukokoma kwake.

4 Kuli mtsinje umene njira zake za madzi zimasangalatsa mzinda wa Mulungu,
malo oyera kumene Wammwambamwamba amakhalako.
5 Mulungu ali m'kati mwake, iwo sudzagwa;
Mulungu adzawuthandiza mmawa.
6 Mitundu ikupokosera, mafumu akugwa;
Iye wakweza mawu ake, dziko lapansi likusungunuka.

7 Yehova Wamphamvuzonse ali ndi ife,
Mulungu wa Yakobo ndi linga lathu.

8 Bwerani kuti mudzaone ntchito za Yehova,
chiwonongeko chimene wachibweretsa pa dziko lapansi.
9 Iye amathetsa nkhondo ku malekezero a dziko lapansi;
Iye amathyola uta ndi kupindapinda mkondo;
amatentha zishango ndi moto.
10 Iye akuti, "Khala chete, ndipo dziwa kuti ndine Mulungu;
ndidzakwezedwa pakati pa mitundu ya anthu;
ine ndidzakwezedwa m'dziko lapansi."

11 Yehova Wamphamvuzonse ali ndi ife,
Mulungu wa Yakobo ndi linga lathu.

# Salimo 47

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la ana a Kora.
1 Ombani m'manja, inu anthu onse;
fuwulani kwa Mulungu ndi mawu achimwemwe.
2 Ndi woopsadi Yehova Wammwambamwamba;
Mfumu yayikulu ya dziko lonse lapansi!
3 Iye anatigonjetsera mitundu yambirimbiri ya anthu;
anayika anthu pansi pa mapazi athu.

4 Iye anatisankhira cholowa chathu,
chonyaditsa cha Yakobo, amene anamukonda.
Sela

5 Mulungu wakwera, anthu akumufuwulira mwachimwemwe,
Yehova wakwera, akumuyimbira malipenga.
6 Imbani matamando kwa Mulungu, imbani matamando;
imbani matamando kwa mfumu yathu, imbani matamando.

7 Pakuti Mulungu ndi mfumu ya dziko lonse lapansi;
imbirani Iye salimo la matamando.
8 Mulungu akulamulira mitundu ya anthu;
Mulungu wakhala pa mpando wake waufumu woyera.
9 Anthu otchuka mwa anthu a mitundu ina asonkhana
monga anthu a Mulungu wa Abrahamu,
pakuti mafumu a dziko lapansi ndi ake a Mulungu;
Iye wakwezedwa kwakukulu.

# Salimo 48

Nyimbo. Salimo la ana a Kora.
1 Wamkulu ndi Yehova, ndi woyenera kwambiri matamando
mu mzinda wa Mulungu wathu, phiri lake loyera.
2 Lokongola mu utali mwake,
chimwemwe cha dziko lonse lapansi.
Malo aatali kwambiri a Zafoni ndiye Phiri la Ziyoni,
mzinda wa Mfumu yayikulu.
3 Mulungu ali mu malinga ake;
Iye wadzionetsa yekha kuti ndiye malinga akewo.

4 Pamene mafumu anasonkhana pamodzi,
pamene anayendera pamodzi kudzalimbana nafe,
5 iwo anaona mzindawo ndipo anadabwa kwambiri;
anathawa ndi mantha aakulu.
6 Pomwepo anagwidwa nako kunjenjemera,
ululu wonga wa mkazi woyembekezera pa nthawi yochira.
7 Inu munawawononga monga sitima zapamadzi za ku Tarisisi
zitawonongeka ndi mphepo ya kummawa.

8 Monga momwe tinamvera,
kotero ife tinaona
mu mzinda wa Yehova Wamphamvuzonse,
mu mzinda wa Mulungu wathu.
Mulungu adzawuteteza kwamuyaya.

9 M'kati mwa Nyumba yanu Mulungu,
ife timalingaliramo zachikondi chanu chosasinthika.
10 Monga dzina lanu, Inu Mulungu,
matamando anu amafika ku malekezero a dziko lapansi
dzanja lanu lamanja ladzaza ndi chilungamo.
11 Phiri la Ziyoni likukondwera,
midzi ya Yuda ndi yosangalala

chifukwa cha maweruzo anu.

12 Yendayendani mu Ziyoni, uzungulireni mzindawo,
werengani nsanja zake.
13 Yang'anitsitsani bwino mipanda yake,
penyetsetsani malinga ake,
kuti mudzafotokoze za izo ku m'bado wotsatira.
14 Pakuti Mulungu uyu ndi Mulungu wathu ku nthawi zosatha;
Iye adzakhala mtsogoleri wathu mpaka ku mapeto.

# Salimo 49

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la ana a Kora.
1 Imvani izi anthu a mitundu yonse;
mvetserani, nonse amene mumakhala pa dziko lonse,
2 anthu wamba pamodzi ndi anthu odziwika,
olemera pamodzinso ndi osauka:
3 Pakamwa panga padzayankhula mawu anzeru;
mawu ochokera mu mtima mwanga adzapereka nzeru.
4 Ndidzatchera khutu langa ku mwambo,
ndi pangwe ndidzafotokoza momveka mwambi wanga.

5 Ine ndichitirenji mantha pamene masiku oyipa afika,
pamene achinyengo oyipa andizungulira.
6 Iwo amene adalira kulemera kwawo
ndi kutamandira kuchuluka kwa chuma chawo?
7 Palibe munthu amene angawombole moyo wa mnzake
kapena kuperekera mnzake dipo kwa Mulungu.
8 Dipo la moyo ndi la mtengowapatali,
palibe malipiro amene angakwanire,
9 kuti iye akhale ndi moyo mpaka muyaya
ndi kusapita ku manda.

10 Pakuti onse amaona kuti anthu anzeru amamwalira;
opusa ndi opanda nzeru chimodzimodzinso amawonongeka
ndipo amasiyira chuma chawo anthu ena.
11 Manda awo adzakhala nyumba zawo mpaka muyaya,
malo awo okhalako kwa nthawi yonse ya mibado yawo,
ngakhale anatchula malo mayina awo.

12 Ngakhale munthu akhale wachuma chotani,
adzafa ngati nyama.

13 Izi ndi zimene zimachitikira iwo amene amadzidalira okha,
ndi owatsatira awo amene amavomereza zimene amayankhula.
Sela
14 Monga nkhosa iwo ayenera kupita ku manda,
ndipo imfa idzawadya.
Olungama adzawalamulira mmawa;
matupi awo adzavunda m'manda,
kutali ndi nyumba zawo zaufumu.
15 Koma Mulungu adzawombola moyo wanga kuchoka ku manda;
ndithu Iye adzanditengera kwa Iye mwini.

16 Usavutike mu mtima pamene munthu akulemera,
pamene ulemerero wa nyumba yake ukuchulukirachulukira;
17 Pakuti sadzatenga kanthu pamodzi naye pamene wamwalira,
ulemerero wake sudzapita pamodzi naye.
18 Ngakhale pamene munthuyo ali moyo amadziyesa wodala,
ndipo ngakhale atamandidwe pamene zinthu zikumuyendera bwino,
19 iyeyo adzakakhala pamodzi ndi m'bado wa makolo ake,
amene sadzaonanso kuwala.

20 Munthu amene ali ndi chuma koma wopanda nzeru
adzafa ngati nyama yakuthengo.

# Salimo 50

Salimo la Asafu.
1 Wamphamvuyo, Yehova Mulungu,
akuyankhula ndi kuyitanitsa dziko lapansi
kuyambira kotulukira dzuwa mpaka kumene limalowera.
2 Kuchokera ku Ziyoni, mokongola kwambiri
Mulungu akuwala.
3 Mulungu wathu akubwera ndipo sadzakhala chete;
moto ukunyeketsa patsogolo pake,
ndipo pomuzungulira pali mphepo yamkuntho
4 Iye akuyitanitsa zamumlengalenga
ndi za pa dziko lapansi kuti aweruze anthu ake.
5 Mundisonkhanitsire okhulupirika anga,
amene anachita pangano ndi ine pochita nsembe.
6 Ndipo mayiko akumwamba akulengeza chilungamo chake,
pakuti Mulungu mwini ndi woweruza.

7 Imvani inu anthu anga, ndipo Ine ndidzayankhula,
iwe Israeli, ndipo Ine ndidzayankhula mokutsutsa;
ndine Mulungu, Mulungu wako.
8 Sindikudzudzula chifukwa cha nsembe zako,
kapena nsembe zako zopsereza zimene zili pamaso panga nthawi zonse.
9 Ine sindikufuna ng'ombe yayimuna kuchokera m'khola lako
kapena mbuzi za m'khola lako,
10 pakuti nyama iliyonse yakunkhalango ndi yanga
ndiponso ng'ombe za ku mapiri ochuluka.
11 Ine ndimadziwa mbalame iliyonse m'mapiri
ndiponso zolengedwa zonse zakutchire ndi zanga.
12 Ndikanakhala ndi njala sindikanakuwuzani,
pakuti dziko lonse ndi zonse zimene zili m'menemo ndi zanga.
13 Kodi ndimadya nyama ya ng'ombe zazimuna
kapena kumwa magazi a mbuzi?
14 "Pereka nsembe zachiyamiko kwa Mulungu,
kwaniritsa malonjezo ako kwa Wammwambamwamba.
15 Ndipo undiyitane pa tsiku lako la masautso;
Ine ndidzakulanditsa, ndipo udzandilemekeza."
16 Koma kwa woyipa, Mulungu akuti,
"Kodi uli ndi mphamvu yanji kuti uzinena malamulo anga
kapena kutenga pangano langa pa milomo yako?

17 Iwe umadana ndi malangizo anga
ndipo umaponyera kumbuyo kwako mawu anga.
18 Ukaona wakuba umamutsatira,
umachita maere ako pamodzi ndi achigololo
19 Umagwiritsa ntchito pakamwa pako pa zinthu zoyipa
ndipo umakonza lilime lako kuchita chinyengo.
20 Nthawi zonse umayankhula motsutsana ndi m'bale wako
ndipo umasinjirira mwana wa amayi ako enieni.
21 Wachita zimenezi ndipo Ine ndinali chete;
umaganiza kuti ndine wofanana nawe
koma ndidzakudzudzula
ndipo ndidzakutsutsa pamaso pako.

22 "Ganizira izi, iwe amene umayiwala Mulungu
kuti ndingakukadzule popanda wokupulumutsa:
23 Iye amene amapereka nsembe yamayamiko amandilemekeza,
ndipo amakonza njira zake kuti ndimuonetse
chipulumutso cha Mulungu."

# Salimo 51

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide. Pamene Mneneri Natani anabwera kwa iye atachita chigololo ndi Batiseba.

1 Mundichitire chifundo, Inu Mulungu,
molingana ndi chikondi chanu chosasinthika;
molingana ndi chifundo chanu chachikulu
mufafanize mphulupulu zanga.
2 Munditsuke zolakwa zanga zonse
ndipo mundiyeretse kuchotsa tchimo langa.

3 Pakuti ndikudziwa mphulupulu zanga,
ndipo tchimo langa lili pamaso panga nthawi zonse.
4 Motsutsana ndi Inu, Inu nokha, ndachimwa
ndipo ndachita zoyipa pamaso panu,
Kotero kuti inu mwapezeka kuti ndinu wolungama
pamene muyankhula ndi pamene muweruza.
5 Zoonadi ine ndinali wochimwa pomwe ndimabadwa,
wochimwa kuyambira pa nthawi imene amayi anga anakhala woyembekezera ine.
6 Zoonadi inu mumafuna choonadi mu ziwalo zam'kati mwanga;
mumandiphunzitsa nzeru m'kati mwanga mwenimweni.

7 Mundiyeretse ndi hisope ndipo ndidzayera,
munditsuke ndipo ndidzayera kuposa matalala
8 Mundilole ndimve chimwemwe ndi chisangalalo,
mulole kuti mafupa amene mwawamphwanya akondwere.
9 Mufulatire machimo anga
ndi kufafaniza zolakwa zanga zonse.

10 Mulenge m'kati mwanga mtima woyera Inu Mulungu
ndi kukonzanso mzimu wokhazikika mwa ine.
11 Musandichotse pamaso panu
kapena kuchotsa Mzimu wanu Woyera mwa ine.

12 Bwezeretsani mwa ine chimwemwe cha chipulumutso chanu
ndipo mundipatse mzimu wofuna kumvera kuti undilimbitse.

13 Pamenepo ndidzaphunzitsa anthu amphulupulu njira zanu
kuti ochimwa adzabwerere kwa inu.
14 Mundipulumutse ku tchimo lokhetsa magazi, Inu Mulungu,
Mulungu wa chipulumutso changa,
ndipo lilime langa lidzayimba zachilungamo chanu.
15 Inu Ambuye tsekulani milomo yanga,
ndipo pakamwa panga padzalengeza matamando anu.
16 Inu simusangalatsidwa ndi nsembe wamba.
Ndikanapereka nsembe yopsereza, Inu simukondwera nayo.
17 Nsembe za Mulungu ndi mzimu wosweka;
mtima wosweka ndi wachisoni
Inu Mulungu simudzawunyoza.

18 Mwa kukoma mtima kwanu mupange Ziyoni kuti alemere;
mumange makoma a Yerusalemu.
19 Kotero kudzakhala nsembe zachilungamo,
nsembe yonse yopsereza yokondweretsa Inu;
ndipo ng'ombe zazimuna zidzaperekedwa pa guwa lanu la nsembe.

# Salimo 52

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe, ndakatulo ya Davide; pamene Doegi Mwedomu anapita kwa Sauli ndi kunena kuti "Davide wapita ku nyumba ya Ahimeleki."

1 N'chifukwa chiyani ukudzitamandira ndi zoyipa, iwe munthu wamphamvu?
N'chifukwa chiyani ukudzitamandira tsiku lonse,
iwe munthu wochititsa manyazi pamaso pa Mulungu?
2 Tsiku lonse umakhalira kuganizira za kuwononga ena;
lilime lako lili ngati lumo lakuthwa,
ntchito yako n'kunyenga.
3 Iwe umakonda choyipa m'malo mwa kuyankhula choonadi.
Umakonda kunama kupambana kuyankhula zoona.
Sela
4 Umakonda mawu onse opweteka,
iwe lilime lachinyengo!

5 Zoonadi Mulungu adzakutsitsa kupita ku chiwonongeko chamuyaya:
iye adzakukwatula ndi kukuchotsa m'tenti yako;
iye adzakuzula kuchoka m'dziko la amoyo.
6 Olungama adzaona zimenezi ndi kuchita mantha;
adzamuseka n'kumanena kuti,
7 "Pano tsopano pali munthu
amene sanayese Mulungu linga lake,
koma anakhulupirira chuma chake chambiri
nalimbika kuchita zoyipa!"

8 Koma ine ndili ngati mtengo wa olivi
wobiriwira bwino m'nyumba ya Mulungu;
ndimadalira chikondi chosatha cha Mulungu

kwa nthawi za nthawi.
9 Ine ndidzakutamandani kwamuyaya chifukwa cha zimene mwachita;
chifukwa cha zimene mwachita; m'dzina lanu ndidzayembekezera
pakuti dzina lanulo ndi labwino. Ndidzakutamandani pamaso pa oyera mtima anu.

# Salimo 53

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a Mahalati. Ndakatulo ya Davide.

1 Chitsiru chimati mu mtima mwake,
"Kulibe Mulungu."
Iwo ndi oyipa ndipo njira zawo ndi zonyansa;
palibe ndi mmodzi yemwe amene amachita chabwino.

2 Mulungu kumwamba amayang'ana pansi pano
pa ana a anthu
kuti aone ngati alipo wina wanzeru,
wofunafuna Mulungu.
3 Aliyense wabwerera,
iwo onse pamodzi akhala oyipa;
palibe ndi mmodzi yemwe amene amachita chabwino,
ngakhale mmodzi.

4 Kodi anthu ochita zoyipawa adzaphunziradi;
anthu amene amadya anthu anga monga mmene anthu amadyera buledi,
ndipo sapemphera kwa Mulungu?
5 Iwo anali pamenepo atathedwa nzeru ndi mantha aakulu
pamene panalibe kanthu kochititsa mantha.
Mulungu anamwazamwaza mafupa a anthu amene anakuthirani nkhondo;
inuyo munawachititsa manyazi, pakuti Mulungu anawanyoza.

6 Ndithu, chipulumutso cha Israeli n'chochokera ku Ziyoni!
Pamene Mulungu adzabwezeretsanso ulemerero wa anthu ake,
lolani Yakobo akondwere ndi Israeli asangalale!

# Salimo 54

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Pa zoyimbira za zingwe. Ndakatulo ya Davide. Pamene anthu a ku Zifi anapita kwa Sauli ndipo anati, "Kodi Davide sakubisala pakati pathu."

1 Pulumutseni Inu Mulungu, mwa dzina lanu;
onetsani kuti ndine wosalakwa mwamphamvu yanu.
2 Imvani pemphero langa, Inu Mulungu
mvetserani mawu a pakamwa panga.

3 Alendo akundithira nkhondo;
anthu ankhanza akufunafuna moyo wanga,
anthu amene salabadira za Mulungu.

4 Zoonadi Mulungu ndi thandizo langa;
Ambuye ndiye amene amandichirikiza ine.

5 Lolani kuti choyipa chifike pa iwo amene amandichita chipongwe;
mwa kukhulupirika kwanu awonongeni.

6 Ine ndidzapereka nsembe yaufulu kwa Inu;
ndidzatamanda dzina lanu, Inu Yehova,
pakuti ndi labwino.
7 Pakuti Iyeyo wandipulumutsa ku masautso anga onse,
ndipo maso anga apenya kupambana kwa pa adani anga.

# Salimo 55

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Ndakatulo ya Davide. Pa zoyimbira za zingwe.

1 Mvetserani pemphero langa, Inu Mulungu,
musakufulatire kupempha kwanga,
2 mverani ndipo mundiyankhe.
Maganizo anga akundisautsa ndipo ndathedwa nzeru
3 chifukwa cha mawu a adani anga,
chifukwa cha kupondereza kwa anthu oyipa;
pakuti andidzetsera masautso
ndipo akundizunza mu mkwiyo wawo.

4 Mtima wanga ukupweteka m’kati mwanga;
mantha a imfa andigwera.
5 Mantha ndi kunjenjemera zandizinga;
mantha aakulu andithetsa nzeru.
6 Ndinati, “Ndithu, ndikanakhala ndi mapiko ankhunda!
Ndikanawulukira kutali ndi kukapuma.
7 Ndikanathawira kutali
ndi kukakhala m’chipululu.
8 Ndikanathamangira kumalo anga a chitetezo;
kutali ndi mphepo yaukali ndi yamkuntho.”

9 Sokonezani maganizo a oyipa, Inu Ambuye, tsutsani mawu awo;
pakuti ine ndikuona chiwawa ndi mkangano mu mzinda.
10 Usana ndi usiku iwo akuzungulirazungulira pa makoma ake;
nkhwidzi ndi kuzunza kuli m’kati mwake.
11 Mphamvu zowononga zili pa ntchito mu mzinda;
kuopseza ndi mabodza sizichoka m’misewu yake.

12 Akanakhala mdani akundinyoza, ine
ndikanapirira;
akanakhala mdani akudzikweza yekha kutsutsana nane,
ndikanakabisala.
13 Koma iweyo mnzanga, mnzanga woyenda naye,
bwenzi langa la pondaapan’pondepo, ndi amene ukuchita zimenezi.
14 Mnzanga amene nthawi ina tinkasangalala
pa chiyanjano chokoma ku nyumba ya Mulungu.

15 Mulole imfa itenge adani anga mwadzidzidzi;
alowe m’manda ali amoyo
pakuti choyipa chili pakati pawo.

16 Koma ine ndinafuwulira kwa Mulungu,
ndipo Yehova anandipulumutsa.
17 Madzulo, mmawa ndi masana
ndimalira mowawidwa mtima,
ndipo Iye amamva mawu anga.
18 Iye amandiwombola ine osavulazidwa
pa nkhondo imene yafika kulimbana nane,
ngakhale kuti ndi ambiri amene akunditsutsa.
19 Mulungu amene ali pa mpando wake kwamuyaya,
adzandimenyera nkhondo; adzawatsitsa adani anga,
chifukwa safuna kusintha njira zawo zoyipa
ndipo saopa Mulungu.

20 Mnzanga woyenda naye wathira nkhondo abwenzi ake;
iye akuphwanya pangano ake.
21 Mawu ake ndi osalala kuposa batala
komabe nkhondo ili mu mtima mwake;
mawu ake ndi osalala kwambiri kuposa mafuta,
komatu mawuwo ndi malupanga osololoka.

22 Tulani nkhawa zanu kwa Yehova
ndipo Iye adzakulimbitsani;
Iye sadzalola kuti wolungama agwe.
23 Koma Inu Mulungu mudzawatsitsa anthu oyipa
kulowa m'dzenje lachiwonongeko;
anthu okhetsa magazi ndi anthu achinyengo
sadzakhala moyo theka la masiku awo,

koma ine ndimadalira Inu.

# Salimo 56

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a "Njiwa pa Mtengo wa Thundu wa Kutali." Mikitamu ya Davide, pamene Afilisti anamugwira ku Gati.

1 Mundichitire chifundo Inu Mulungu, pakuti anthu akundithamangitsa kwambiri;
tsiku lonse akundithira nkhondo.
2 Ondinyoza akundithamangitsa tsiku lonse,
ambiri akumenyana nane monyada.

3 Ndikachita mantha
ndimadalira Inu.
4 Mwa Mulungu, amene mawu ake ine ndimatamanda,
mwa Mulungu ine ndimadaliramo; sindidzachita mantha.
Kodi munthu amene amafa angandichite chiyani?

5 Tsiku lonse amatembenuza mawu anga;
nthawi zonse amakonza zondivulaza.
6 Iwo amakambirana, amandibisalira,
amayang'anitsitsa mayendedwe anga
ndipo amakhala ndi chidwi chofuna kuchotsa moyo wanga.

7 Musalole konse kuti athawe;
mu mkwiyo wanu Mulungu mugwetse mitundu ya anthu.
8 Mulembe za kulira kwanga,
mulembe chiwerengero cha misozi yanga m'buku lanu.
Kodi zimenezi sizinalembedwe m'buku lanulo?

9 Adani anga adzabwerera m'mbuyo
pamene ndidzalirira kwa Inu.
Pamenepo ndidzadziwa kuti Mulungu ali ku mbali yanga.
10 Mwa Mulungu amene mawu ake ndimawatamanda,
mwa Yehova amene mawu ake ndimawatamanda,
11 mwa Mulungu ine ndimadalira ndipo sindidzachita mantha.
Kodi munthu angandichite chiyani?

12 Ndiyenera kuchita zomwe ndinalumbira kwa Mulungu;
ndidzapereka nsembe zanga zachiyamiko kwa inu.
13 Pakuti mwawombola moyo wanga ku imfa
ndi mapazi anga kuti ndingagwe,
kuti ndiyende pamaso pa Mulungu
m'kuwala kwa moyo.

# Salimo 57

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a "Musawononge." Ndakatulo ya Davide, pamene anathawa Sauli kupita ku phanga.

1 Mundichitire chifundo, Inu Mulungu mundichitire chifundo,
pakuti mwa Inu moyo wanga umathawiramo.
Ndidzathawira mu mthunzi wa mapiko anu
mpaka chiwonongeko chitapita.

2 Ine ndikufuwulira kwa Mulungu Wammwambamwamba,
kwa Mulungu amene amakwaniritsa cholinga chake pa ine.
3 Mulungu amanditumizira kuchokera kumwamba ndi kundipulumutsa,
kudzudzula iwo amene akundithamangitsa kwambiri.
Mulungu amatumiza chikondi chake ndi kukhulupirika kwake.

4 Ine ndili pakati pa mikango,
ndagona pakati pa zirombo zolusa;
anthu amene mano awo ndi milomo yawo ndi mivi,
malilime awo ndi malupanga akuthwa.

5 Mukwezekedwe Inu Mulungu, kuposa mayiko onse akumwamba;
mulole kuti ulemerero wanu ukhale pa dziko lonse lapansi.

6 Iwo anatchera mapazi anga ukonde
ndipo ndinawerama pansi mosautsidwa.
Anakumba dzenje m'njira yanga
koma agweramo okha m'menemo.

7 Mtima wanga ndi wokhazikika, Inu Mulungu
mtima wanga ndi wokhazikika.
Ndidzayimba nyimbo, nyimbo yake yamatamando.
8 Dzuka moyo wanga!

Dzukani zeze ndi pangwe!
Ndidzadzuka m’bandakucha.

9 Ndidzakutamandani Ambuye, pakati pa mitundu ya anthu,
ndidzayimba za Inu pakati pa mayiko.
10 Pakuti chikondi chanu n’chachikulu, kufikira ku mayiko akumwamba;
kukhulupirika kwanu kwafika ku mitambo.

11 Mukwezekedwe Inu Mulungu kuposa mayiko akumwamba,
mulole kuti ulemerero wanu ukhale pa dziko lonse lapansi.

# Salimo 58

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a “Musawononge.” Ndakatulo ya Davide.

1 Kodi inu olamulira mumayankhuladi molungama?
Kodi mumaweruza mwachilungamo pakati pa anthu?
2 Ayi, m’mitima mwanu mumakonzekera zosalungama,
ndipo manja anu amatulutsa zachiwawa pa dziko lapansi.
3 Ngakhale kuchokera tsiku lawo lobadwa oyipa amasochera;
kuchokera m’mimba ya amayi awo, iwo ndi otayika ndipo amayankhula mabodza.
4 Ululu wawo uli ngati ululu wa njoka,
ngati uja wa mphiri imene yatseka m’makutu mwake.
5 Imene simva liwu la munthu wamatsenga,
ngakhale akhale wa luso lotani munthu wamatsengayo.

6 Gululani mano m’kamwa mwawo, Inu Mulungu,
Yehova khadzulani mano a mikango!
7 Mulole kuti asowe ngati madzi oyenda
pamene iwo akoka uta mulole kuti mivi yawo ikhale yosathwa.
8 Akhale ngati nkhono imene imasungunuka pamene ikuyenda;
ngati mwana wakufa asanabadwe, iwo asaone dzuwa.

9 Miphika yanu isanagwire moto waminga ya mkandankhuku,
kaya iyo ndi yobiriwira kapena yowuma, oyipa adzachotsedwa.
10 Olungama adzasangalala poona kubwezera chilango,
pamene adzasambitsa mapazi awo m’magazi a anthu oyipa.
11 Ndipo anthu adzanena kuti,
“Zoonadi, olungama amalandirabe mphotho;
zoonadi kuli Mulungu amene amaweruza dziko lapansi.”

# Salimo 59

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a “Musawononge.” Ndakatulo ya Davide. Pamene Sauli anatumiza anthu kuti akalondere nyumba ya Davide ndi cholinga choti amuphe.

1 Landitseni kwa adani anga, Inu Mulungu;
munditeteze kwa anthu amene auka kutsutsana nane.
2 Landitseni kwa anthu ochita zoyipa
ndipo mundipulumutse kwa anthu okhetsa magazi.

3 Onani momwe iwo akundibisalira!
Anthu owopsa agwirizana zolimbana nane;

osati chifukwa cha mlandu kapena tchimo langa, Inu Yehova.
4 Ine sindinachite cholakwa, koma iwo ndi okonzeka kundithira nkhondo.
Dzukani kuti mundithandize; penyani mavuto anga!
5 Inu Yehova Mulungu Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli,
dzidzutseni nokha kuti mulange anthu a mitundu ina yonse;
musaonetse chifundo chanu kwa anthu oyipa achinyengowa.

6 Iwo amabweranso madzulo
akuchita phokoso ngati agalu
ndi kumangoyendayenda mu mzinda.
7 Onani zomwe amalavula m'kamwa mwawo;
iwo amalavula malupanga kuchokera pa milomo yawo,
ndipo amanena kuti, "Ndani angatimve?"
8 Koma Inu Yehova, mumawaseka,
mumayinyoza mitundu yonseyo.

9 Inu mphamvu yanga, ine ndiyang'ana kwa inu;
Inu Mulungu, ndinu linga langa. 10 Mulungu wanga wachikondi.

Mulungu adzapita patsogolo panga
ndipo adzandilola kunyada pa iwo amene amandinyoza.
11 Koma musawaphe, Inu Ambuye chishango chathu,
kuopa kuti anthu anga angayiwale.
Mwa mphamvu zanu,
lolani kuti azingoyendayenda ndipo muwatsitse.
12 Chifukwa cha machimo a pakamwa pawo
chifukwa cha mawu a milomo yawo,
iwo akodwe m'kunyada kwawo.
Chifukwa cha matemberero ndi mabodza amene ayankhula
13 muwawononge mu ukali (wanu)
muwawononge mpaka atheretu.
Pamenepo zidzadziwika ku malekezero a dziko lapansi
kuti Mulungu amalamulira Yakobo.

14 Iwo amabweranso madzulo,
akuchita phokoso ngati agalu
ndi kumangoyenda mu mzinda.
15 Iwo amayendayenda kufuna chakudya
ndipo amawuwa ngati sanakhute.
16 Koma ine ndidzayimba za mphamvu yanu,
mmawa ndidzayimba zachikondi chanu;
pakuti ndinu linga langa,
pothawirapo panga m'nthawi ya mavuto.

17 Inu mphamvu yanga, ndiyimba matamando kwa inu;
Inu Mulungu, ndinu linga langa, Mulungu wanga wachikondi.

# Salimo 60

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a "Kakombo wa Pangano." Mikitamu ya Davide yophunzitsira. Pamene anamenyana ndi Mesopotamiya ndi Aramu-Zoba, ndi pamene Yowabu anabwerera ndi kukantha Aedomu 12,000 m'Chigwa cha Mchere.

1 Inu Mulungu mwatikanatu ife, ndipo mwatiwonongera otiteteza.
Inu mwatikwiyira, tsopano tibwezeretseni mwakale!
2 Inu mwagwedeza dziko ndipo mwaling'amba,
konzani ming'alu yake pakuti ikugwedezeka kwambiri.
3 Inu mwaonetsa anthu anu nthawi za mavuto;
inu mwatipatsa vinyo amene watichititsa kudzandira.

4 Koma kwa iwo amene amaopa Inu, Inu mwakweza mbendera
kuti tisonkhanireko pothawa uta.

5 Tipulumutseni ndi kutithandiza ndi dzanja lanu lamanja,
kuti iwo amene mumawakonda apulumutsidwe.
6 Mulungu wayankhula kuchokera ku malo ake opatulika:
"Mwakupambana ndidzagawa Sekemu
ndipo ndidzayeza malire a chigwa cha Sukoti.
7 Giliyadi ndi wanga, Manase ndi wanganso;
Efereimu ndi chipewa changa chodzitetezera,
Yuda ndi ndodo yanga yaufumu
8 Mowabu ndi mbale yanga yosambira,
pa Edomu ndidzaponyapo nsapato yanga,
pa Filisitiya ndidzafuwula mwakupambana."

9 Adzandifikitse ndani ku mzinda wotetezedwa?
Ndani adzanditsogolera ku Edomu?
10 Kodi si Inu Mulungu, Inu amene mwatikana ife
ndipo simutuluka pamodzi ndi magulu athu ankhondo.
11 Tipatseni chithandizo kuti tilimbane ndi mdani wathu,
pakuti thandizo lochokera kwa munthu ndi lopanda phindu.
12 Chifukwa cha Mulungu, ife tidzapeza chipambano
ndipo tidzapondaponda adani athu.

# Salimo 61

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide. Loyimbidwa ndi zipangizo za zingwe.

1 Imvani kulira kwanga, Inu Mulungu;
mvetserani pemphero langa.

2 Kuchokera ku malekezero a dziko lapansi ine ndimayitana Inu
ndimayitana pomwe mtima wanga ukufowoka;
tsogolereni ku thanthwe lalitali kuposa ineyo.
3 Pakuti Inu mwakhala pothawirapo panga,
nsanja yolimba polimbana ndi adani anga.

4 Ine ndikulakalaka kukhala m'tenti yanu kwamuyaya
ndi kupeza chitetezo mu mthunzi wa mapiko anu.
5 Pakuti Inu Mulungu mwamva malumbiro anga;
mwandipatsa cholowa cha iwo amene amaopa dzina lanu.

6 Wonjezerani masiku a moyo wa mfumu,
zaka zake kwa mibado yochuluka.
7 Iye akhale pa mpando waufumu pamaso pa Mulungu kwamuyaya;

ikani chikondi chanu ndi kukhulupirika kwanu kuti zimuteteze.

8 Kotero ndidzayimba matamando kwamuyaya pa dzina lanu
ndi kukwaniritsa malumbiro anga tsiku ndi tsiku.

# Salimo 62

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Kutsata mayimbidwe a Yedutuni. Salimo la Davide.

1 Moyo wanga umapeza mpumulo mwa Mulungu yekha;
chipulumutso changa chimachokera kwa Iye.
2 Iye yekhayo ndiye thanthwe langa ndi chipulumutso changa;
Iye ndi linga langa, choncho sindidzagwedezeka.

3 Kodi nonsenu mudzalimbana naye munthu mpaka liti?
Kodi mudzamugwetsa pansi ngati khoma losalimba,
ngati mpanda wogwedezeka?
4 Iwo akufunitsitsa kumugwetsa
kuti achoke pa malo ake apamwamba.
Iwo amakondweretsedwa ndi mabodza.
Ndi pakamwa pawo amadalitsa
koma m'mitima yawo amatemberera.

5 Peza mpumulo mwa Mulungu yekhayo iwe moyo wanga;
chiyembekezo changa chichokera mwa Iye.
6 Iye yekhayo ndiye thanthwe langa ndi chipulumutso changa;
Iyeyo ndi linga langa; sindidzagwedezeka.
7 Chipulumutso changa ndi ulemu wanga zimachokera kwa Mulungu:
Iye ndiye thanthwe langa lamphamvu; Mulungu ndiye pothawira panga.
8 Dalirani Iye nthawi zonse, inu anthu;
khuthulani mitima yanu kwa Iye,
pakuti Mulungu ndiye pothawirapo pathu.
Sela

9 Anthu wamba ndi mpweya chabe;
anthu apamwamba ndi bodza chabe;
ngati atayezedwa pa sikelo iwo ndi chabe;
iwowo pamodzi ndi mpweya ndi chabe
10 Musadalire kulanda mwachinyengo
kapena katundu wobedwa;
ngakhale chuma chanu chichuluke,
musayike mtima wanu pa icho.

11 Mulungu wayankhula kamodzi,
ine ndamvapo zinthu ziwiri;
choyamba n'chakuti Inu Mulungu ndinu wamphamvu,
12 komanso Inu Ambuye, chikondi chanu n'chosasinthika.
Chachiwiri n'chakuti mumamuchitira munthu
molingana ndi ntchito zake.

# Salimo 63

Salimo la Davide. Pamene anali m'chipululu cha Yuda.

1 Inu Mulungu, ndinu Mulungu wanga,
moona mtima ine ndimakufunafunani;
moyo wanga uli ndi ludzu lofuna Inu,
thupi langa likulakalaka inu,
m'dziko lowuma ndi lotopetsa
kumene kulibe madzi.

2 Inu ndinakuonani ku malo anu opatulika
ndipo ndinapenya mphamvu zanu ndi ulemerero wanu.
3 Chifukwa chikondi chanu
ndi choposa moyo, milomo yanga idzakulemekezani.
4 Ndidzakutamandani masiku onse a moyo wanga,
ndipo m'dzina lanu ndidzakweza manja anga.
5 Mudzakhutitsa moyo wanga ndi zonona.
Ine ndidzakutamandani ndi mawu anthetemya.

6 Pa bedi panga ndimakumbukira inu;
ndimaganiza za Inu nthawi yonse ya usiku.
7 Chifukwa ndinu thandizo langa,
ine ndimayimba mu mthunzi wa mapiko anu.
8 Moyo wanga umakangamira Inu;
dzanja lanu lamanja limandigwiriziza.

9 Iwo amene akufunafuna moyo wanga adzawonongedwa;
adzatsikira kunsi kozama kwa dziko lapansi.
10 Iwo adzaperekedwa ku lupanga
ndi kukhala chakudya cha ankhandwe.

11 Koma mfumu idzakondwera mwa Mulungu;
onse amene amalumbira m'dzina la Mulungu adzalemekeza Mulunguyo,
koma pakamwa pa anthu onama padzatsekedwa.

# Salimo 64

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Ndimvereni Mulungu pomwe ndikunena madandawulo anga;
tetezani moyo wanga ku chiopsezo cha mdani.
2 Ndibiseni ku chiwembu cha anthu oyipa,
ku gulu laphokoso la anthu ochita zoyipa.

3 Iwo amanola malilime awo ngati malupanga,
amaponya mawu awo olasa ngati mivi.
4 Iwo amaponya mivi yawo ali pa malo wobisala kwa munthu wosalakwa;
amamulasa modzidzimutsa ndi mopanda mantha.

5 Iwo amalimbikitsana wina ndi mnzake pa chikonzero chawo choyipa,
amayankhula zobisa misampha yawo;
ndipo amati, "Adzayiona ndani?"
6 Iwo amakonzekera zosalungama ndipo amati,
"Takonza ndondomeko yabwino kwambiri!"
Ndithu maganizo ndi mtima wa munthu ndi zachinyengo.

7 Koma Mulungu adzawalasa ndi mivi;
mwadzidzidzi adzakanthidwa.
8 Iye adzatembenuza milomo yawoyo kuwatsutsa
ndi kuwasandutsa bwinja;
onse amene adzawaona adzagwedeza mitu yawo mowanyoza.

9 Anthu onse adzachita mantha;
adzalengeza ntchito za Mulungu
ndi kulingalira mozama zomwe Iye wazichita.
10 Lolani wolungama akondwere mwa Yehova
ndi kubisala mwa Iye,
owongoka mtima onse atamande Iye!

# Salimo 65

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide. Nyimbo.
1 Matamando akudikira Inu Mulungu mu Ziyoni;
kwa inu malumbiro athu adzakwaniritsidwa.
2 Inu amene mumamva pemphero,
kwa inu anthu onse adzafika.
3 Pamene tinathedwa nzeru ndi machimo,
Inu munakhululukira mphulupulu zathu.
4 Odala iwo amene inu muwasankha
ndi kuwabweretsa pafupi kukhala m'mabwalo anu!
Ife tadzazidwa ndi zinthu zabwino za m'Nyumba mwanu,
za m'Nyumba yanu yoyera.

5 Mumatiyankha ife ndi ntchito zodabwitsa zachilungamo,
Inu Mulungu Mpulumutsi wathu,
chiyembekezo cha mathero onse a dziko lapansi
ndi cha nyanja zomwe zili kutali kwambiri,
6 amene munapanga mapiri ndi mphamvu zanu,
mutadziveka nokha ndi mphamvu.
7 Amene munakhalitsa bata nyanja
kukokoma kwa mafunde ake,
ndi phokoso la anthu a mitundu ina.
8 Iwo amene akukhala kutali amaopa zizindikiro zozizwitsa zanu;
kumene dzuwa limatulukira ndi kumene dzuwa limalowera.
Inu mumafuna nyimbo zachimwemwe.

9 Inu mumasamalira dziko lapansi ndi kulithirira;
Inuyo mumalilemeretsa kwambiri.
Mtsinje wa Mulungu ndi wodzaza ndi madzi
kuti upereke tirigu kwa anthu,
pakuti Inu munakhazikitsa zimenezi.
10 Mwadzaza nthaka yake ndi madzi ndi kusalaza migula yake,
mwayifewetsa ndi mvula yamawawa ndi kudalitsa mbewu zake.
11 Inu mumaveka chaka ndi zinthu zochuluka,
ndipo ngolo zanu zimasefukira ndi zinthu zochuluka.
12 Malo a udzu a m'chipululu amasefukira;
mapiri avekedwa ndi chisangalalo.
13 Madambo akutidwa ndi zoweta
ndi zigwa zavekedwa ndi tirigu;

izo pamodzi zikufuwula ndi kuyimba mwachimwemwe.

# Salimo 66

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo.

1 Fuwulani kwa Mulungu ndi chimwemwe, dziko lonse lapansi!
2 Imbani ulemerero wa dzina lake;
kumutamanda kwake kukhale kwaulemerero.
3 Nenani kwa Mulungu, “Ntchito zanu ndi zoopsa ndithu!
Mphamvu yanu ndi yayikulu kwambiri
kotero kuti adani anu amawerama pamaso panu.
4 Dziko lonse lapansi limaweramira inu;
limayimba matamando kwa Inu;
limayimba matamando pa dzina lanu.”
Sela.

5 Bwerani mudzaone zimene Mulungu wachita,
ntchito zanu ndi zoopsa ndithu pakati pa anthu.
6 Iye anasandutsa nyanja kukhala malo owuma,
iwo anawoloka pa madzi ndi mapazi.
Bwerani, tiyeni tikondwere mwa Iye.
7 Iye amalamulira ndi mphamvu zake mpaka muyaya,
maso ake amayang’anira anthu a mitundu ina.
Anthu owukira asadzitukumule.

8 Tamandani Mulungu wathu, inu mitundu ya anthu,
mulole kuti mawu a matamando ake amveke;
9 Iye watchinjiriza miyoyo yathu
ndi kusunga mapazi athu kuti angaterereke.
10 Pakuti Inu Mulungu munatiyesa;
munatiyenga ngati siliva.
11 Inu mwatilowetsa m’ndende
ndi kutisenzetsa zolemera pa misana yathu.
12 Inu munalola kuti anthu akwere pa mitu yathu;
ife tinadutsa m’moto ndi m’madzi,
koma Inu munatibweretsa ku malo a zinthu zochuluka.

13 Ine ndidzabwera ku Nyumba yanu ndi nsembe zopsereza
ndi kukwaniritsa malumbiro anga.
14 Malumbiro amene milomo yanga inalonjeza
ndi pakamwa panga panayankhula pamene ndinali pa mavuto.
15 Ndidzapereka nsembe nyama zonenepa kwa Inu
ndi chopereka cha nkhosa zazimuna;
ndidzapereka ng’ombe zamphongo ndi mbuzi.
Sela

16 Bwerani ndipo mudzamve inu nonse amene mumaopa Mulungu.
Ndidzakuwuzani zimene Iyeyo wandichitira.
17 Ndinafuwula kwa Iye ndi pakamwa panga,
matamando ake anali pa lilime panga.
18 Ndikanasekerera tchimo mu mtima mwanga
Ambuye sakanamvera;
19 koma ndithu Mulungu wamvetsera

ndipo watchera khutu ku mawu a kupempha kwanga.
20 Matamando akhale kwa Mulungu
amene sanakane pemphero langa
kapena kuletsa chikondi chake pa ine!

# Salimo 67

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Pa zoyimbira za zingwe. Salimo.
1 Yehova atikomere mtima ndi kutidalitsa,
achititse kuti nkhope yake itiwalire.
2 Kuti njira zanu zidziwike pa dziko lapansi,
chipulumutso chanu pakati pa mitundu yonse.

3 Mitundu ya anthu ikutamandeni Inu Mulungu;
mitundu yonse ya anthu ikutamandeni.
4 Mitundu yonse ya anthu isangalale ndi kuyimba mwachimwemwe,
pakuti inu mumaweruza mitundu ya anthu mwachilungamo
ndi kutsogolera mitundu ya anthu a dziko lapansi.
5 Mitundu ya anthu ikutamandeni Inu Mulungu;
mitundu yonse ya anthu ikutamandeni.

6 Nthaka yabereka zokolola zake;
tidalitseni Mulungu wathu.
7 Mulungu atidalitse
kuti pamenepo malekezero onse a dziko lapansi apembedze Iyeyo.

# Salimo 68

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Adzuke Mulungu, adani ake amwazikane;
adani ake athawe pamaso pake.
2 Monga momwe mphepo imachotsera utsi; Inu muwawulutsire kutali.
Monga phula limasungunukira pa moto,
oyipa awonongeke pamaso pa Mulungu.
3 Koma olungama asangalale
ndi kukondwera pamaso pa Mulungu;
iwo akondwere ndi kusangalala.

4 Imbirani Mulungu imbirani dzina lake matamando,
mukwezeni Iye amene amakwera pa mitambo;
dzina lake ndi Yehova ndipo sangalalani pamaso pake.
5 Atate wa ana amasiye, mtetezi wa akazi amasiye,
ndiye Mulungu amene amakhala m’malo oyera.
6 Mulungu amakhazikitsa mtima pansi osungulumwa m’mabanja,
amatsogolera am’ndende ndi kuyimba;
koma anthu osamvera amakhala ku malo owuma a dziko lapansi.

7 Pamene munatuluka kutsogolera anthu anu, Inu Mulungu,
pamene munayenda kudutsa chipululu,
8 dziko lapansi linagwedezeka, miyamba inakhuthula pansi mvula,
pamaso pa Mulungu, Mmodzi uja wa ku Sinai.
Pamaso pa Mulungu, Mulungu wa Israeli.
9 Munapereka mivumbi yochuluka, Inu Mulungu;

munatsitsimutsa cholowa chanu cholefuka.
10 Anthu anu anakhala m’menemo
ndipo munapatsa anthu osauka zimene zinkawasowa chifukwa cha ubwino wanu Mulungu.

11 Ambuye analengeza mawu,
ndipo gulu linali lalikulu la iwo amene anapita kukawafalitsa;
12 “Mafumu ndi ankhondo anathawa mwaliwiro;
m’misasa anthu anagawana zolanda pa nkhondo.
13 Ngakhale mukugona pakati pa makola a ziweto,
mapiko a nkhunda akutidwa ndi siliva,
nthenga zake ndi golide wonyezimira.”
14 Pamene Wamphamvuzonse anabalalitsa mafumu m’dziko,
zinali ngati matalala akugwa pa Zalimoni.

15 Mapiri a Basani ndi mapiri aulemerero;
mapiri a Basani, ndi mapiri a msonga zambiri.
16 Muyang’aniranji mwansanje inu mapiri a msonga zambiri,
pa phiri limene Mulungu analisankha kuti azilamulira,
kumene Yehova mwini adzakhalako kwamuyaya?
17 Magaleta a Mulungu ndi osawerengeka,
ndi miyandamiyanda;
Ambuye wabwera kuchokera ku Sinai, walowa m’malo ake opatulika.
18 Pamene Inu munakwera mmwamba,
munatsogolera a m’ndende ambiri;
munalandira mphatso kuchokera kwa anthu,
ngakhale kuchokera kwa owukira,
kuti Inu Mulungu, mukhale kumeneko.

19 Matamando akhale kwa Ambuye, kwa Mulungu Mpulumutsi wathu
amene tsiku ndi tsiku amasenza zolemetsa zathu.
20 Mulungu wathu ndi Mulungu amene amapulumutsa;
Ambuye Wamphamvuzonse ndiye amene amatipulumutsa ku imfa.

21 Ndithu Mulungu adzaphwanya mitu ya adani ake,
zipewa za ubweya za iwo amene amapitiriza kuchita machimo awo.
22 Ambuye akunena kuti, “Ndidzawabweretsa kuchokera ku Basani;
ndidzawabweretsa kuchokera ku nyanja zozama.
23 Kuti muviyike mapazi anu m’magazi a adani anu,
pamene malilime a agalu anu akudyapo gawo lawo.”

24 Mayendedwe aulemu a anthu anu aonekera poyera, Inu Mulungu;
mayendedwe olemekeza Mulungu wanga ndi Mfumu yanga yokalowa m’malo opatulika.
25 Patsogolo pali oyimba nyimbo pakamwa, pambuyo pawo oyimba nyimbo ndi zipangizo;
pamodzi ndi iwo pali atsikana akuyimba matambolini.
26 Tamandani Mulungu mu msonkhano waukulu;
tamandani Yehova mu msonkhano wa Israeli.
27 Pali fuko laling’ono la Benjamini, kuwatsogolera,
pali gulu lalikulu la ana a mafumu a Yuda,
ndiponso pali ana a mafumu a Zebuloni ndi Nafutali.

28 Kungani mphamvu zanu Mulungu;
tionetseni nyonga zanu, Inu Mulungu, monga munachitira poyamba.
29 Chifukwa cha Nyumba yanu ku Yerusalemu,
mafumu adzabweretsa kwa Inu mphatso.
30 Dzudzulani chirombo pakati pa mabango,
gulu la ng'ombe zazimuna pakati pa ana ang'ombe a mitundu ya anthu.
Mochititsidwa manyazi, abweretse mitanda ya siliva.
Balalitsani anthu a mitundu ina amene amasangalatsidwa ndi nkhondo.
31 Nthumwi zidzachokera ku Igupto;
Kusi adzadzipereka yekha kwa Mulungu.

32 Imbirani Mulungu Inu mafumu a dziko lapansi
imbirani Ambuye matamando.

Sela

33 Kwa Iye amene amakwera pa mitambo yakalekale ya mmwamba
amene amabangula ndi mawu amphamvu.
34 Lengezani za mphamvu za Mulungu,
amene ulemerero wake uli pa Israeli
amene mphamvu zake zili m'mitambo.
35 Ndinu woopsa, Inu Mulungu m'malo anu opatulika;
Mulungu wa Israeli amapereka mphamvu ndi nyonga kwa anthu ake.

Matamando akhale kwa Mulungu!

# Salimo 69

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide. Potsata mayimbidwe a "Akakombo."

1 Pulumutseni Inu Mulungu,
pakuti madzi afika m'khosi
2 Ine ndikumira m'thope lozama
m'mene mulibe popondapo.
Ndalowa m'madzi ozama;
mafunde andimiza.
3 Ndafowoka ndikupempha chithandizo;
kummero kwanga kwawuma gwaa,
m'maso mwanga mwada
kuyembekezera Mulungu wanga.
4 Iwo amene amadana nane popanda chifukwa
ndi ochuluka kuposa tsitsi la kumutu kwanga;
ambiri ndi adani anga popanda chifukwa,
iwo amene akufunafuna kundiwononga.
Ndikukakamizidwa kubwezera
zomwe sindinabe.

5 Mukudziwa uchitsiru wanga, Inu Mulungu,
kulakwa kwanga sikuli kobisika kwa Inu.

6 Iwo amene amadalira Inu
asanyozedwe chifukwa cha ine,
Inu Ambuye Wamphamvuzonse.
Iwo amene amafunafuna Inu

asachititsidwe manyazi chifukwa cha ine,
Inu Mulungu wa Israeli.
7 Pakuti ndimapirira kunyozedwa chifukwa cha Inu,
ndipo manyazi amaphimba nkhope yanga.
8 Ndine mlendo kwa abale anga,
munthu wakudza kwa ana aamuna a amayi anga;
9 pakuti changu chochitira nyumba yanu chandiphetsa
ndipo chipongwe cha iwo amene amanyoza Inu chandigwera.
10 Pamene ndikulira ndi kusala kudya,
ndiyenera kupirira kunyozedwa;
11 pomwe ndavala chiguduli,
anthu amandiseweretsa.
12 Iwo amene amakhala pa chipata amandinena,
ndipo ine ndine nyimbo ya zidakwa.

13 Koma ndikupempha kwa Inu Ambuye,
pa nthawi yanu yondikomera mtima;
mwa chikondi chanu chachikulu
Inu Mulungu, mundiyankhe pondipulumutsa.
14 Mundilanditse kuchoka m'matope,
musalole kuti ndimire,
pulumutseni ine kwa iwo
amene amadana nane, kuchoka m'madzi ozama.
15 Musalole kuti chigumula chindimeze,
kuya kusandimeze
ndipo dzenje lisatseke pakamwa pake kundimiza.
16 Ndiyankheni Inu Yehova mwa ubwino wanu wa chikondi chanu;
mwa chifundo chanu chachikulu tembenukirani kwa ine.
17 Musabisire nkhope yanu mtumiki wanu,
ndiyankheni msanga, pakuti ndili pa mavuto.
18 Bwerani pafupi ndi kundilanditsa;
ndiwomboleni chifukwa cha adani anga.

19 Inu mukudziwa momwe ndanyozedwera,
kunyozedwa ndi kuchititsidwa manyazi; adani anga onse ali pamaso panu.
20 Mnyozo waswa mtima wanga
ndipo wandisiya wopanda thandizo lililonse;
ndinafunafuna ena woti andichitire chisoni,
koma panalibe ndi mmodzi yemwe woti anditonthoze, sindinapeze ndi mmodzi yemwe.
21 Iwo anayika ndulu m'chakudya changa
ndi kundipatsa vinyo wosasa chifukwa cha ludzu.

22 Chakudya chomwe chayikidwa patsogolo pawo chikhale msampha;
chikhale chobwezera chilango ndiponso khwekhwe.
23 Maso awo adetsedwe kotero kuti asaonenso
ndipo misana yawo ipindike mpaka kalekale.
24 Khuthulirani ukali wanu pa iwo;
mkwiyo wanu woyaka moto uwathe mphamvu.
25 Malo awo akhale wopanda anthu
pasapezeke ndi mmodzi yemwe wokhala m'matenti awo.

26 Pakuti iwo amazunza amene inu munamuvulaza
ndi kuyankhula zowawa kwa amene munawapweteka.
27 Awonjezereni kulakwa pa kulakwa kwawo,
musalole kuti akhale ndi gawo pa chipulumutso chanu.
28 Iwo afufutidwe m'buku la amoyo
ndipo asalembedwe pamodzi ndi olungama.

29 Ndikumva zowawa ndi kuzunzika;
lolani chipulumutso chanu, Inu Mulungu, chinditeteze.

30 Ine ndidzatamanda dzina la Mulungu m'nyimbo,
ndidzalemekeza Iye ndi chiyamiko.
31 Izi zidzakondweretsa Yehova kupambana ng'ombe,
kupambananso ng'ombe yayimuna, pamodzi ndi nyanga ndi ziboda zake.
32 Wosauka adzaona ndipo adzasangalala,
Inu amene mumafunafuna Mulungu, mitima yanu ikhale ndi moyo!
33 Yehova amamvera anthu osowa
ndipo sanyoza anthu ake omangidwa.

34 Kumwamba ndi dziko lapansi zitamanda Iye,
nyanja ndi zonse zomwe zimayenda m'menemo,
35 pakuti Mulungu adzapulumutsa Ziyoni
ndi kumanganso mizinda ya Yuda,
anthu adzakhala kumeneko ndipo dzikolo lidzakhala lawo;
36 ana atumiki ake adzalitenga kukhala cholowa chawo,
ndipo iwo amene amakonda dzina lake adzakhala kumeneko.

# Salimo 70

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide. Pempho.

1 Fulumirani Mulungu kundipulumutsa;
Yehova bwerani msanga kudzandithandiza.
2 Iwo amene akufunafuna moyo wanga
achititsidwe manyazi ndi kusokonezedwa;
onse amene akukhumba chiwonongeko changa
abwezedwe mopanda ulemu.
3 Onse amene akunena kwa ine kuti, "Aha, aha,"
abwerere chifukwa cha manyazi awo.
4 Koma onse amene akufunafuna Inu
akondwere ndi kusangalala mwa Inu;
iwo amene amakonda chipulumutso chanu
nthawi zonse anene kuti, "Mulungu akuzike!"

5 Koma ine ndine wosauka ndi wosowa;
bwerani msanga kwa ine Inu Mulungu.
Inu ndinu thandizo langa ndi momboli wanga;
Inu Yehova musachedwe.

# Salimo 71

1 Mwa Inu Yehova ine ndathawiramo;
musalole kuti ndichititsidwe manyazi.
2 Mundilanditse ndi kundipulumutsa mwa chilungamo chanu,

mutchere khutu lanu ndi kundipulumutsa.
3 Mukhale thanthwe langa lothawirapo,
kumene ine nditha kupita nthawi zonse;
lamulani kuti ndipulumuke,
pakuti Inu ndinu thanthwe langa ndi linga langa.
4 Landitseni Inu Mulungu wanga, kuchoka m'dzanja la oyipa,
kuchoka m'dzanja la oyipa ndi anthu ankhanza.

5 Pakuti Inu mwakhala chiyembekezo changa, Inu Ambuye Wamphamvuzonse,
chilimbikitso changa kuyambira ndili mwana.
6 Kuyambira pamene ndinabadwa, ndakhala ndikudalira Inu;
Inu munanditulutsa m'mimba mwa amayi anga,
ndipo ndidzakupembedzani nthawi zonse.
7 Ine ndakhala chinthu chodabwitsa kwa anthu ambiri
koma Inu ndinu wonditchinjiriza wamphamvu.
8 Pakamwa panga padzaza ndi matamando anu,
kulengeza ulemerero wanu tsiku lonse.

9 Musanditaye pamene ndakalamba;
musandisiye pamene mphamvu zanga zatha.
10 Pakuti adani anga ayankhula motsutsana nane;
iwo amene amadikira kuti andiphe amapangana pamodzi.
11 Iwo amati, "Mulungu wamusiya;
mutsatireni ndi kumugwira,
pakuti palibe amene adzamupulumutse."
12 Musakhale kutali ndi ine Inu Mulungu,
bwerani msanga, Inu Mulungu wanga; thandizeni.
13 Ondineneza anga awonongeke mwa manyazi,
iwo amene akufuna kundipweteka
avale chitonzo ndi manyazi.

14 Koma ine ndidzakhala ndi chiyembekezo mwa Inu nthawi zonse,
ndidzakutamandani mowirikizawirikiza.
15 Pakamwa panga padzafotokoza za chilungamo chanu,
za chipulumutso chanu tsiku lonse,
ngakhale sindikudziwa muyeso wake.
16 Ndidzabwera ndi kulengeza za machitidwe amphamvu zanu Inu Ambuye Wamphamvuzonse.
Ndidzalengeza chilungamo chanu, chanu chokha.
17 Kuyambira ubwana wanga, Inu Mulungu mwakhala mukundiphunzitsa,
ndipo mpaka lero ine ndikulengeza za ntchito zanu zodabwitsa
18 Ngakhale pamene ndakalamba ndipo imvi zili mbuu
musanditaye Inu Mulungu,
mpaka nditalengeza mphamvu zanu
kwa mibado yonse yakutsogolo.

19 Mphamvu zanu ndi kulungama kwanu zimafika mpaka kumwambamwamba.
Ndani wofanana nanu Inu Mulungu,
amene mwachita zazikulu?
20 Ngakhale mwandionetsa mavuto

ambiri owawa,
mudzabwezeretsanso moyo wanga;
kuchokera kunsi kwa dziko lapansi,
mudzandiukitsanso.
21 Inu mudzachulukitsa ulemu wanga
ndi kunditonthozanso.

22 Ndidzakutamandani ndi zeze
chifukwa cha kukhulupirika kwanu Mulungu,
ndidzayimba matamando kwa Inu ndi pangwe,
Inu Woyera wa Israeli.
23 Milomo yanga idzafuwula ndi chimwemwe
pamene ndidzayimba matamando kwa Inu
amene mwandiwombola.
24 Lilime langa lidzafotokoza za ntchito zanu zachilungamo
tsiku lonse,
pakuti iwo amene amafuna kundipweteka
achititsidwa manyazi ndi kusokonezedwa.

# Salimo 72

Salimo la Solomoni.
1 Patsani mwana wa mfumu nzeru zanu zoweruzira mwa chilungamo,
Inu Mulungu mupatseni mwana wa mfumu chilungamo chanu.
2 Iye adzaweruza anthu anu mwachilungamo,
anthu anu ozunzika mosakondera.
3 Mapiri adzabweretsa chuma kwa anthu anu,
timapiri tidzabweretsa zipatso zachilungamo.
4 Iye adzateteza ozunzika pakati pa anthu
ndi kupulumutsa ana a anthu osowa;
adzaphwanya ozunza anzawo.

5 Adzakhala ndi moyo pa mibado yonse,
nthawi zonse pamene dzuwa ndi mwezi zikuwala.
6 Iye adzakhala kugwa kwa mvula pa minda yolimidwa
ngati mivumbi yothirira dziko lapansi.
7 M’masiku a munthu wolungama adzakhazikika;
chuma chidzachuluka mpaka mwezi utaleka kuwala.

8 Iye adzalamulira kuchokera ku nyanja ina mpaka ku nyanja ina
ndiponso kuchokera ku mtsinje mpaka ku malekezero a dziko lapansi.
9 Mafuko a m’chipululu adzawerama pamaso pake
ndipo adani ake adzanyambita fumbi.
10 Mafumu a ku Tarisisi ndi a ku zilumba zakutali
adzabweretsa mitulo kwa iye,
mafumu a ku Seba ndi Seba
adzapereka mphatso kwa iyeyo.
11 Mafumu onse adzamuweramira
ndipo mitundu yonse idzamutumikira.

12 Pakuti iye adzawombola wosowa amene akulira,
wozunzika amene alibe wina womuthandiza.
13 Iye adzachitira chifundo anthu ofowoka ndi anthu osowa

ndi kupulumutsa osowa ku imfa.
14 Iye adzalanditsa iwo ku mazunzo ndi chiwawa
pakuti magazi awo ndi amtengo wapatali pamaso pake.

15 Iye akhale ndi moyo wautali;
golide ochokera ku Seba apatsidwe kwa iye.
Anthu amupempherere nthawi zonse
ndi kumudalitsa tsiku lonse.
16 Mulole kuti tirigu achuluke m'dziko lonse;
pamwamba pa mapiri pakhale tirigu.
Zipatso zake zichuluke ngati za ku Lebanoni;
zichuluke ngati udzu wakuthengo
17 Dzina lake likhazikike kwamuyaya,
lipitirire kukhala monga momwe limakhalira dzuwa.

Mitundu yonse idzadalitsika kudzera mwa iye
ndipo iwo adzamutcha iye wodala.

18 Matamando akhale kwa Yehova Mulungu, Mulungu wa Israeli
amene Iye yekha amachita ntchito zodabwitsa.
19 Matamando akhale ku dzina lake laulemerero kwamuyaya
dziko lonse lapansi lidzaze ndi ulemerero wake.
Ameni ndi Ameni.

20 Uku ndiko kumaliza kwa mapemphero a Davide mwana wa Yese.

# BUKU LACHITATU

## 73

*Masalimo 73–89*

Salimo la Asafu.
1 Mulungu ndi wabwino ndithu kwa Israeli,
kwa iwo amene ndi oyera mtima.

2 Koma kunena za ine, mapazi anga anali pafupi kuterereka;
ndinatsala pang'ono kugwa.
3 Pakuti ndinkachitira nsanje odzitamandira,
pamene ndinaona mtendere wa anthu oyipa.

4 Iwo alibe zosautsa;
matupi awo ndi athanzi ndi amphamvu.
5 Saona mavuto monga anthu ena;
sazunzika ngati anthu ena onse.
6 N'chifukwa chake kunyada kuli monga mkanda wa m'khosi mwawo;
amadziveka chiwawa.
7 M'mitima yawo yokhota mumachokera zolakwa;
zoyipa zochokera m'maganizo awo sizidziwa malire.
8 Iwowo amanyogodola ndi kumayankhula zoyipa;
mwa kudzikuza kwawo amaopseza ena n'kumati, "Tikuponderezani."
9 Pakamwa pawo pamayankhula monyoza Mulungu kumwamba
ndipo lilime lawo limayenda pa dziko lapansi.
10 N'chifukwa chake anthu awo amapita kwa iwowo
ndi kumwa madzi mochuluka.

11 Iwo amati, “Kodi Mulungu angadziwe bwanji?
Kodi Wammwambamwamba angadziwe kalikonse?”

12 Umu ndi mmene oyipa alili;
nthawi zonse ali pabwino ndipo chuma chawo chimachulukirachulukira.

13 Ndithudi ine ndawusunga pachabe mtima wanga woyera;
pachabe ndasamba m’manja mwanga mwa kusalakwa kwanga.
14 Tsiku lonse ndapeza mavuto;
ndakhala ndi kulangidwa mmawa uliwonse.

15 Ndikanati, “Ndidzayankhula motere,”
ndikanachita chosakhulupirika kwa ana anu.
16 Pamene ndinayesa kuti ndimvetse zonsezi,
zinandisautsa kwambiri
17 kufikira nditalowa m’malo opatulika a Mulungu;
pamenepo ndinamvetsa mathero awo.

18 Zoonadi Inu munawayika pa malo woterera;
Mumawagwetsa pansi kuti awonongeke.
19 Mwamsangamsanga iwo amawonongedwa,
amasesedwa kwathunthu ndi mantha!
20 Monga loto pamene wina adzuka,
kotero pamene Inu muuka, Inu Ambuye,
mudzawanyoza ngati maloto chabe.

21 Pamene mtima wanga unasautsidwa
ndi kuwawidwa mu mzimu mwanga,
22 ndinali wopusa ndi wosadziwa;
ndinali chirombo chopanda nzeru pamaso panu.

23 Komabe ineyo ndili ndi Inu nthawi zonse;
mumandigwira dzanja langa lamanja.
24 Inu mumanditsogolera ndi malangizo anu
ndipo pambuyo pake mudzanditenga ku ulemerero.
25 Kodi kumwamba ndili ndi yani kupatula Inu?
Ndipo dziko lapansi lilibe chilichonse chimene ndimachilakalaka koposa Inuyo.
26 Thupi ndi mtima wanga zitha kufowoka,
koma Mulungu ndiye mphamvu ya mtima wanga
ndi cholandira changa kwamuyaya.

27 Iwo amene ali kutali ndi Inu adzawonongeka;
Inu mumawononga onse osakhulupirika pamaso panu.
28 Koma kunena za Ine ndi kwabwino kukhala pafupi ndi Mulungu.
Ndatsimikiza kuti Ambuye Yehova ndiwo pothawirapo panga
ndipo ndidzalalika ntchito zanu zonse.

# Salimo 74

Ndakatulo ya Asafu.
1 N’chifukwa chiyani mwatitaya ife kwamuyaya, Inu Mulungu?

Chifukwa chiyani mkwiyo wanu ukutukutira pa nkhosa za busa lanu?
2 Kumbukirani anthu amene munawagula kalekale,
fuko la cholowa chanu, limene Inu munaliwombola,
phiri la Ziyoni, kumene inuyo mumakhala.
3 Tembenuzani mapazi kuloza ku mabwinja awa amuyaya
chiwonongeko ichi chonse mdani wabweretsa pa malo opatulika.

4 Adani anu anabangula pa malo pamene Inu munkakumana nafe;
anayimika mbendera zawo monga zizindikiro zachigonjetso.
5 Iwo anachita ngati anthu oti anyamula mbendera zawo
kuti adule mitengo m'nkhalango.
6 Kenaka anaphwanya ndi nkhwangwa ndi akasemasema awo
zonse zimene tinapachika.
7 Iwo anatentha malo anu opatulika mpaka kuwagwetsa pansi;
anadetsa malo okhalamo dzina lanu.
8 Ndipo anati m'mitima yawo, "Tawatha kwathunthu."
Anatentha malo aliwonse amene Mulungu amapembedzedwerako m'dzikomo.
9 Ife sitinapatsidwe chizindikiro chodabwitsa;
palibe aneneri amene atsala
ndipo palibe aliyense wa ife akudziwa kuti izi zidzatenga nthawi yayitali bwanji.

10 Kodi mpaka liti, mdani adzanyoze Inu Mulungu?
Kodi amaliwongowa adzapeputsa dzina lanu kwamuyaya?
11 Chifukwa chiyani mukubweza dzanja lanu lamanja?
Litulutseni kuchoka pachifuwa chanu ndipo muwawononge!

12 Koma Inu Mulungu, ndinu Mfumu yanga kuyambira kalekale;
Mumabweretsa chipulumutso pa dziko lapansi.
13 Ndinu amene munagawa nyanja ndi mphamvu yanu;
munathyola mitu ya zirombo za m'madzi.
14 Ndinu amene munaphwanya mitu ya Leviyatani
ndi kuyipereka ngati chakudya cha zirombo za m'chipululu.
15 Ndinu amene munatsekula akasupe ndi mitsinje,
munawumitsa mitsinje imene siphwa nthawi zonse.
16 Masana ndi anu ndipo usiku ndi wanunso;
Inuyo munakhazikitsa dzuwa ndi mwezi.
17 Ndinu amene munakhazikitsa malire onse a dziko lapansi;
munakhazikitsa chilimwe ndi dzinja.

18 Kumbukirani momwe mdani wakunyozerani Inu Yehova,
momwe anthu opusa apeputsira dzina lanu.
19 Musapereke moyo wa nkhunda yanu ku zirombo zakuthengo;
nthawi zonse musayiwale miyoyo ya anthu anu osautsidwa.
20 Mukumbukire pangano lanu, pakuti malo obisika a m'dziko
asanduka mochitira zachiwawa zochuluka.
21 Musalole kuti osautsidwa abwerere mwamanyazi;
osauka ndi osowa atamande dzina lanu.

22 Dzukani Inu Mulungu ndipo dzitetezeni pa mlandu;
kumbukirani momwe opusa akukunyozerani tsiku lonse.

23 Musalekerere phokoso la otsutsana nanu,
chiwawa cha adani anu, chimene chikumveka kosalekeza.

# Salimo 75

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe, potsata mayimbidwe a "Musawononge." Salimo la Asafu. Nyimbo.

1 Tikuthokoza Inu Mulungu,
tikuthokoza, pakuti dzina lanu lili pafupi nafe,
anthutu amafotokoza za ntchito zanu zodabwitsa.

2 Mumati, "Ine ndimayika nthawi yoyenera,
ndine amene ndimaweruza mwachilungamo.
3 Pamene dziko lapansi ndi anthu ake onse anjenjemera,
ndine amene ndimagwiriziza mizati yake molimba.
Sela
4 Kwa odzitama ndikuti, 'Musadzitamenso,'
ndipo kwa oyipa, 'Musatukulenso nyanga zanu.
5 Musatukule nyanga zanu motsutsana ndi kumwamba;
musayankhule ndi khosi losololoka.' "

6 Kugamula milandu sikuchokera kummawa kapena kumadzulo
kapena ku chipululu.
7 Koma ndi Mulungu amene amaweruza:
Iyeyo amatsitsa wina, nakwezanso wina.
8 M'dzanja la Yehova muli chikho
chodzaza ndi vinyo wochita thovu, wosakanizidwa ndi zokometsera;
Iye amamutsanulira pansi ndipo onse oyipa a dziko lapansi
amamwa ndi senga zake zonse.

9 Kunena za ine, ndidzalengeza izi kwamuyaya;
ndidzayimba matamando kwa Mulungu wa Yakobo.
10 Ndidzadula nyanga za onse oyipa
koma nyanga za olungama zidzakwezedwa.

# Salimo 76

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Pa zoyimbira za zingwe. Salimo la Asafu.

1 Mulungu amadziwika mu Yuda;
dzina lake ndi lotchuka mu Israeli.
2 Tenti yake ili mu Salemu,
malo ake okhalamo mu Ziyoni.
3 Kumeneko Iye anathyola mivi yowuluka,
zishango ndi malupanga, zida zankhondo.
Sela

4 Wolemekezeka ndinu,
wamphamvu kuposa mapiri amene ali ndi nyama zambiri.
5 Anthu owuma mtima amagona atalandidwa chuma,
Iwowo amagona tulo tawo totsiriza;
palibe mmodzi wamphamvu
amene angatukule manja ake.
6 Pa kudzudzula kwanu, Inu Mulungu wa Yakobo,

kavalo pamodzi ndi galeta zimakhala chete zitagona pansi.
7 Inu nokha ndiye muyenera kuopedwa.
Angathe kuyima pamaso panu ndani mukakwiya?
8 Kuchokera kumwamba Inu munalengeza chiweruzo,
ndipo dziko linaopa ndi kukhala chete,
9 pamene Inu Mulungu munadzuka kuti muweruze,
kupulumutsa onse osautsidwa m'dziko.
Sela
10 Zoonadi, ukali wanu pa anthu umakubweretserani matamando
ndipo opulumuka ku ukali wanu mumawasunga pafupi nanu.

11 Chitani malumbiro kwa Yehova Mulungu wanu ndipo muwakwaniritse;
anthu onse omuzungulira abweretse mphatso
kwa Iye amene ayenera kuopedwa.
12 Iye amaswa mzimu wa olamulira;
amaopedwa ndi mafumu a dziko lapansi.

# Salimo 77

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a Yedutuni. Salimo la Asafu.

1 Ndinafuwulira Mulungu kupempha thandizo;
ndinafuwula mokweza kwa Mulungu kuti anditcherere khutu.
2 Pamene ndinali pa masautso ndinafunafuna Ambuye;
usiku ndinatambasula manja mosalekeza
ndipo moyo wanga unakana kutonthozedwa.

3 Ndinakumbukira Inu Mulungu, ndipo ndinabuwula;
ndinasinkhasinkha ndipo mzimu wanga unalefuka.
Sela
4 Munagwira zikope zanga kuti ndisagone
ndipo ndinavutika kwambiri kuti ndiyankhule.
5 Ndinaganizira za masiku akale,
zaka zamakedzana;
6 Ndinakumbukira nyimbo zanga usiku.
Mtima wanga unasinkhasinkha ndipo mzimu wanga unafunsa kuti,

7 "Kodi Ambuye adzatikana mpaka muyaya?
Kodi Iwo sadzaonetsanso kukoma mtima kwawo?
8 Kodi Chikondi chake chosatha chija chatheratu?
Kodi malonjezo ake alephera nthawi yonse?
9 Kodi Mulungu wayiwala kukhala wokoma mtima?
Kodi mu mkwiyo wake waleka chifundo chake?"

10 Ndipo ndinaganiza, "Pa izi ine ndidzapemphanso:
zaka za dzanja lamanja la Wammwambamwamba.
11 Ine ndidzakumbukira ntchito za Yehova;
Ine ndidzakumbukira zodabwitsa zanu za kalekale.
12 Ndidzakumbukira ntchito zanu
ndi kulingalira zodabwitsa zanu."

13 Njira zanu Mulungu ndi zoyera.
Kodi ndi mulungu uti ali wamkulu kuposa Mulungu wathu?

14 Inu ndinu Mulungu wochita zodabwitsa;
Mumaonetsera mphamvu yanu pakati pa mitundu ya anthu.
15 Ndi dzanja lanu lamphamvu munawombola anthu anu,
zidzukulu za Yakobo ndi Yosefe.
Sela

16 Madzi anakuonani Mulungu,
madzi anakuonani ndipo anachita mantha;
nyanja yozama inakomoka.
17 Mitambo inakhuthula madzi ake pansi,
mu mlengalenga munamveka mabingu;
mivi yanu inawuluka uku ndi uku.
18 Bingu lanu linamveka m'mphepo ya kamvuluvulu,
mphenzi yanu inawalitsa dziko lonse;
dziko lapansi linanjenjemera ndi kugwedezeka.
19 Njira yanu inadutsa pa nyanja,
njira yanu inadutsa pa madzi amphamvu,
ngakhale zidindo za mapazi anu sizinaoneke.

20 Inu munatsogolera anthu anu ngati gulu la nkhosa
mwa dzanja la Mose ndi Aaroni.

# Salimo 78

Ndakatulo ya Asafu.
1 Inu anthu anga imvani chiphunzitso changa;
mvetserani mawu a pakamwa panga.
2 Ndidzatsekula pakamwa panga m'mafanizo,
ndidzayankhula zinthu zobisika, zinthu zakalekale
3 zimene tinazimva ndi kuzidziwa,
zimene makolo athu anatiwuza.
4 Sitidzabisira ana awo,
tidzafotokozera m'bado wotsatira
ntchito zotamandika za Yehova,
mphamvu zake, ndi zozizwitsa zimene Iye wachita.
5 Iye anapereka mawu wodzichitira umboni kwa Yakobo
ndi kukhazikitsa lamulo mu Israeli,
zimene analamulira makolo athu
kuphunzitsa ana awo,
6 kotero kuti m'bado wotsatira uthe kuzidziwa,
ngakhale ana amene sanabadwe,
ndi kuti iwo akafotokozere ana awonso.
7 Choncho iwo adzakhulupirira Mulungu
ndipo sadzayiwala ntchito zake
koma adzasunga malamulo ake.
8 Iwo asadzakhale monga makolo awo,
m'bado wosamvera ndi wowukira,
umene mitima yake inali yosamvera Mulungu,
umene mizimu yake inali yosakhulupirika kwa Iye.

9 Anthu a ku Efereimu, ngakhale ananyamula mauta,
anathawabe pa nthawi ya nkhondo;
10 iwo sanasunge pangano la Mulungu

ndipo anakana kukhala m’moyo wotsatira lamulo lake.
11 Anayiwala zimene Iye anachita,
zozizwitsa zimene anawaonetsa.
12 Iyeyo anachita zodabwitsa makolo athu akuona,
m’dziko la Igupto, m’chigawo cha Zowani.
13 Anagawa nyanja pakati ndi kudutsitsapo iwowo,
Iye anachititsa madzi kuyima chilili ngati khoma.
14 Anawatsogolera ndi mtambo masana
ndi kuwala kwa moto usiku wonse.
15 Iye anang’amba miyala m’chipululu
ndi kuwapatsa madzi ochuluka ngati a m’nyanja zambiri;
16 Anatulutsa mitsinje kuchokera m’ming’alu ya miyala
ndi kuyenda madzi ngati mitsinje.

17 Komabe iwowo anapitiriza kumuchimwira Iye,
kuwukira Wammwambamwamba m’chipululu.
18 Ananyoza Mulungu mwadala
pomuwumiriza kuti awapatse chakudya chimene anachilakalaka.
19 Iwo anayankhula motsutsana naye ponena kuti,
“Kodi Mulungu angatipatse chakudya m’chipululu?
20 Iye atamenya thanthwe
madzi anatuluka,
ndipo mitsinje inadzaza ndi madzi.
Koma iye angatipatsenso ife chakudya?
Kodi angapereke nyama kwa anthu akewa?”
21 Yehova atawamva anakwiya kwambiri;
moto wake unayaka kutsutsana ndi Yakobo,
ndipo mkwiyo wake unauka kutsutsana ndi Israeli,
22 pakuti iwo sanakhulupirire Mulungu
kapena kudalira chipulumutso chake.
23 Komabe Iye anapereka lamulo kwa mitambo mmwamba
ndi kutsekula makomo a mayiko akumwamba;
24 anagwetsa mana kuti anthu adye,
anawapatsa tirigu wakumwamba.
25 Anthu anadya buledi wa angelo,
Iye anawatumizira chakudya chonse chimene akanatha kudya.
26 Anamasula mphepo ya kummwera kuchokera kumwamba,
ndi kutsogolera mphepo ya kummwera mwa mphamvu zake.
27 Iye anawagwetsera nyama ngati fumbi,
mbalame zowuluka ngati mchenga wa m’mbali mwa nyanja.
28 Anazibweretsa kwa iwo m’kati mwa misasa yawo,
kuzungulira matenti awo onse.
29 Iwo anadya mpaka anatsala nazo zochuluka
pakuti Iye anawapatsa zimene anazilakalaka.
30 Koma iwowo anasiya kudya chakudya anachilakalakacho,
chakudya chili m’kamwa mwawobe,
31 mkwiyo wa Mulungu unawayakira;
Iye anapha amphamvu onse pakati pawo,
kugwetsa anyamata abwino kwambiri mu Israeli.

32 Ngakhale zinali chomwechi, iwo anapitirira kuchimwa;
ngakhale anaona zozizwitsa zakezo iwowo sanakhulupirirebe.

33 Kotero Mulungu anachepetsa masiku awo kuti azimirire ngati mpweya.
Iye anachepetsa zaka zawo kuti zithere m'masautso.
34 Mulungu atawapha, iwo amamufunafuna Iyeyo;
iwo ankatembenukiranso kwa Iye mwachangu.
35 Ankakumbukira kuti Mulungu ndiye Thanthwe lawo,
kuti Mulungu Wammwambamwamba ndiye Mpulumutsi wawo.
36 Komabe ankamuthyasika ndi pakamwa pawo,
kumunamiza ndi malilime awo;
37 Mitima yawo sinali yokhazikika pa Iye,
iwo sanakhulupirike ku pangano lake.
38 Komabe Iye anali wachifundo;
anakhululukira mphulupulu zawo
ndipo sanawawononge.
Nthawi ndi nthawi Iye anabweza mkwiyo wake
ndipo sanawutse ukali wake wonse.
39 Iye anakumbukira kuti iwo anali anthu chabe,
mphepo yopita imene sibwerereranso.

40 Nthawi zambiri iwo ankamuwukira Iye m'chipululu
ndi kumumvetsa chisoni m'dziko lopanda kanthu!
41 Kawirikawiri iwo ankamuyesa Mulungu;
ankamuputa Woyera wa Israeli.
42 Sanakumbukire mphamvu zake,
tsiku limene Iye anawawombola kwa ozunza,
43 tsiku limene Iyeyo anaonetsa poyera zizindikiro zozizwitsa zake mu Igupto,
zozizwitsa zake m'chigawo cha Zowani.
44 Iye anasandutsa mitsinje yawo kukhala magazi;
Iwo sanathe kumwa madzi ochokera m'mitsinje yawo.
45 Iye anawatumizira magulu a ntchentche zimene zinawawononga,
ndiponso achule amene anawasakaza.
46 Iye anapereka mbewu zawo kwa ziwala,
zokolola zawo kwa dzombe.
47 Iye anawononga mphesa zawo ndi matalala
ndiponso mitengo yawo yankhuyu ndi chisanu.
48 Iye anapereka ng'ombe zawo ku matalala,
zoweta zawo ku zing'aning'ani.
49 Anakhuthula moto wa ukali wake pa iwo,
anawapsera mtima nawakwiyira n'kuwabweretsera masautso.
Zimenezi zinali ngati gulu la angelo osakaza.
50 Analolera kukwiya,
sanawapulumutse ku imfa
koma anawapereka ku mliri.
51 Anakantha ana oyamba kubadwa a Igupto,
zipatso zoyamba kucha za mphamvu zawo m'matenti a Hamu
52 Koma Iye anatulutsa anthu ake ngati ziweto;
anawatsogolera ngati nkhosa kudutsa m'chipululu.
53 Anawatsogolera bwinobwino kotero kuti analibe mantha
koma nyanja inamiza adani awo.
54 Kotero anawafikitsa ku malire a dziko lake loyera,
ku dziko lamapiri limene dzanja lake lamanja linawatengera.
55 Iye anathamangitsa mitundu ya anthu patsogolo pawo

ndipo anapereka mayiko awo kwa Aisraeli kuti akhale awo;
Iye anakhazikitsa mafuko a Israeli m'nyumba zawo.

56 Koma iwo anayesa Mulungu
ndi kuwukira Wammwambamwamba;
sanasunge malamulo ake.
57 Anakhala okanika ndi osakhulupirika monga makolo awo,
anapotoka monga uta wosakhulupirika.
58 Anakwiyitsa Iyeyo ndi malo awo opembedzera mafano;
anawutsa nsanje yake ndi mafano awo.
59 Pamene Mulungu anamva zimenezi, anakwiya kwambiri;
Iye anakana Israeli kwathunthu.
60 Anasiya nyumba ya ku Silo,
tenti imene Iyeyo anayimanga pakati pa anthu.
61 Anatumiza mphamvu zake ku ukapolo,
ulemerero wake m'manja mwa adani.
62 Anapereka anthu ake ku lupanga;
anakwiya kwambiri ndi cholowa chake.
63 Moto unanyeketsa anyamata awo,
ndipo anamwali awo analibe nyimbo za ukwati;
64 ansembe awo anaphedwa ndi lupanga,
ndipo amayi awo amasiye sanathe kulira.

65 Kenaka Ambuye anakhala ngati akudzuka kutulo,
ngati munthu wamphamvu wofuwula chifukwa cha vinyo.
66 Iye anathamangitsa adani ake;
anawachititsa manyazi ku nthawi zonse.
67 Kenaka Iye anakana matenti a Yosefe,
sanasankhe fuko la Efereimu;
68 Koma anasankha fuko la Yuda,
phiri la Ziyoni limene analikonda.
69 Iye anamanga malo ake opatulika ngati zitunda,
dziko limene analikhazikitsa kwamuyaya.
70 Anasankha Davide mtumiki wake
ndi kumuchotsa pakati pa makola ankhosa;
71 kuchokera koyang'anira nkhosa anamubweretsa
kuti akhale m'busa wa anthu ake, Yakobo,
wa Israeli cholowa chake.
72 Ndipo Davide anawaweta ndi mtima wolungama;
ndi manja aluso anawatsogolera.

# Salimo 79

Salimo la Asafu.
1 Inu Mulungu, anthu a mitundu ina alowerera m'cholowa chanu;
ayipitsa Nyumba yanu yoyera,
asandutsa Yerusalemu kukhala bwinja.
2 Iwo anapereka mitembo ya atumiki anu
kwa mbalame zamlengalenga ngati chakudya,
matupi a oyera mtima anu kwa zirombo za dziko lapansi.
3 Akhetsa magazi monga madzi
kuzungulira Yerusalemu yense,

ndipo palibe wina woti ayike m’manda anthu akufa.
4 Ife ndife chinthu chonyozeka kwa anansi athu,
chosekets a ndi cholalatiridwa kwa iwo amene atizungulira.

5 Mpaka liti Inu Yehova? Kodi mudzakwiya mpaka muyaya?
Kodi mpaka liti nsanje yanu idzayaka ngati moto?
6 Khuthulirani ukali wanu pa anthu a mitundu ina
amene sakudziwani Inu,
pa maufumu
amene sayitana pa dzina lanu;
7 pakuti iwo ameza Yakobo
ndi kuwononga dziko lawo.
8 Musatilange chifukwa cha machimo a makolo athu
chifundo chanu chibwere msanga kukumana nafe,
pakuti tili ndi chosowa chachikulu.

9 Tithandizeni Inu Mulungu Mpulumutsi wathu,
chifukwa cha ulemerero wa dzina lanu;
tipulumutseni ndi kutikhululukira machimo athu
chifukwa cha dzina lanu.
10 Chifukwa chiyani anthu a mitundu ina akuti,
“Ali kuti Mulungu wawo?”
Ife tikuona, zidziwike pakati pa anthu a mitundu ina
kuti mumabwezera chilango chifukwa cha magazi amene
anakhetsedwa a atumiki anu.
11 Kubuwula kwa anthu a m’ndende kufike pamaso panu;
ndi mphamvu ya dzanja lanu
muwasunge amene aweruzidwa kuti aphedwe.

12 Mubwezere kwa anansi athu kasanu n’kawiri
kunyoza kumene ananyoza Inu Ambuye.
13 Pamenepo ife anthu anu, nkhosa za pabusa panu,
tidzakutamandani kwamuyaya,
kuchokera m’bado ndi m’bado
tidzafotokoza za matamando anu.

# Salimo 80

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a “Kakombo wa Pangano.” Salimo la Asafu.
1 Tcherani khutu Inu m’busa wa Israeli,
Inu amene mumatsogolera Yosefe monga nkhosa;
Inu amene mumakhala pa mpando waufumu pakati pa akerubi, walani
2 kwa Efereimu, Benjamini ndi Manase.
Utsani mphamvu yanu;
bwerani ndi kutipulumutsa.

3 Tibwezereni mwakale Inu Mulungu;
nkhope yanu itiwalire
kuti tipulumutsidwe.

4 Inu Mulungu Wamphamvuzonse,
mpaka liti mkwiyo wanu udzanyeka

kutsutsana ndi mapemphero a anthu anu?
5 Mwawadyetsa buledi wa misozi;
mwachitisa iwo kumwa misozi yodzaza mbale.
6 Mwachititsa kuti tikhale gwero la mikangano pakati pa anansi athu,
ndipo adani athu akutinyoza.

7 Tibwezereni mwakale Inu Mulungu Wamphamvuzonse,
nkhope yanu itiwalire
kuti tipulumutsidwe.

8 Munatulutsa mpesa kuchoka ku Igupto;
munathamangitsa anthu a mitundu ina ndi kuwudzala mpesawo.
9 Munawulimira munda wamphesawo,
ndipo unamera ndi kudzaza dziko.
10 Mapiri anaphimbidwa ndi mthunzi wake,
mikungudza yamphamvu ndi nthambi zake.
11 Unatambalitsa nthambi zake mpaka ku nyanja,
mphukira zake mpaka ku mtsinje.

12 Chifukwa chiyani mwagwetsa makoma ake
kuti onse amene akudutsa athyole mphesa zake?
13 Nguluwe zochokera m'nkhalango zikuwononga
ndipo zirombo za mthengo zimawudya.
14 Bweraninso kwa ife Inu Mulungu Wamphamvuzonse!
Yang'anani pansi muli kumwambako ndipo muone!
Uyang'anireni mpesa umenewu,
15 muzu umene dzanja lanu lamanja ladzala,
mwana amene inu munamukuza nokha.

16 Mpesa wanu wadulidwa ndi kutenthedwa ndi moto;
pakudzudzula kwanu anthu anu awonongeka.
17 Dzanja lanu likhale pa munthu amene ali ku dzanja lanu lamanja,
mwana wa munthu amene mwalera nokha.
18 Ndipo ife sitidzatembenukira kumbali kuchoka kwa Inu;
titsitsimutseni ndipo tidzayitana pa dzina lanu.

19 Tibwezereni mwakale Inu Yehova Mulungu Wamphamvuzonse
nkhope yanu itiwalire
kuti tipulumutsidwe.

## Salimo 81

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a gititi. Salimo la Asafu.
1 Imbani mwachimwemwe kwa Mulungu mphamvu yathu;
Fuwulani mokweza kwa Mulungu wa Yakobo!
2 Yambani nyimbo, imbani tambolini
imbani pangwe wolira bwino ndi zeze.

3 Imbani lipenga la nyanga ya nkhosa yayimuna pa mwezi watsopano,
ndi pamene mwezi waoneka wonse, pa tsiku la phwando;
4 ili ndi lamulo kwa Israeli,
langizo la Mulungu wa Yakobo.

5 Iye anapereka lamulolo kwa zidzukulu za Yosefe
pamene anatuluka kulimbana ndi Igupto,
kumene tinamva chiyankhulo chimene sitinachidziwe.

6 Iye akunena kuti, “Ine ndinachotsa zolemetsa pa mapewa awo;
Manja awo anamasulidwa m’dengu.
7 Pa mavuto anu munayitana ndipo ndinakulanditsani,
ndinakuyankhani kuchokera m’mitambo ya mabingu;
ndinakuyesani pa madzi a ku Meriba.
Sela

8 “Imvani anthu anga, ndipo ndidzakuchenjezani
ngati mungathe kumvetsera, Inu Israeli!
9 Musadzakhale ndi mulungu wachilendo pakati panu;
musadzagwadire mulungu wina.
10 Ine ndine Yehova Mulungu wanu,
amene ndinakutulutsani m’dziko la Igupto.
Yasamani kukamwa kwanu ndipo ndidzakudyetsani.

11 “Koma anthu anga sanandimvere;
Israeli sanandigonjere.
12 Kotero ndinawasiya ndi mitima yawo yosamverayo
kuti atsate zimene ankafuna.

13 “Anthu anga akanangondimvera,
Israeli akanatsatira njira zanga,
14 n’kanafulumira motani kuti ndigonjetse adani awo
ndi kutembenuza mkono wanga kulimbana ndi amaliwongo!
15 Iwo amene amadana ndi Yehova akanakhwinyata pamaso pake,
ndipo chilango chawo chinakakhala mpaka kalekale.
16 Koma inu mukanadyetsedwa tirigu wabwino kwambiri;
ndikanakukhutitsani ndi uchi wochokera pa thanthwe.”

# Salimo 82

Salimo la Asafu.
1 Mulungu akutsogolera msonkhano waukulu;
Iye akuweruza pakati pa “milungu.”

2 “Mudzateteza osalungama mpaka liti,
ndi kukondera anthu oyipa?
3 Tetezani anthu ofowoka ndi amasiye;
mukhazikitse ufulu wa anthu osauka ndi ozunzika.
4 Landitsani anthu ofowoka ndi osowa;
apulumutseni m’dzanja la anthu oyipa.

5 “Iwo sadziwa kanthu, sazindikira kalikonse.
Amayendayenda mu mdima;
maziko onse a dziko lapansi agwedezeka.

6 “Ndinati, ‘Inu ndinu Mulungu,
nonsenu ndinu ana a Wammwambamwamba.’
7 Koma mudzafa ngati anthu wamba;

mudzagwa ngati wolamula wina aliyense."

8 Dzukani Inu Mulungu, weruzani dziko lapansi,
pakuti mayiko onse ndi cholowa chanu.

# Salimo 83

Nyimbo. Salimo la Asafu.

1 Inu Mulungu musakhale chete;
musangoti phee, Mulungu musangoti duu.
2 Onani adani anu akuchita chiwawa,
amene amadana nanu autsa mitu yawo.
3 Mochenjera iwo akukambirana za chiwembu kutsutsana ndi anthu anu;
Iwo akukonzekera kutsutsana ndi omwe mumawakonda.
4 Iwo akunena kuti, "Bwerani" akutero, "Tiyeni tiwononge mtundu wonsewu
kuti dzina la Israeli lisakumbukikenso."

5 Ndi mtima umodzi akukonzekera chiwembu;
Iwo achita mgwirizano kutsutsana nanu:
6 Matenti a Edomu ndi Aismaeli,
Mowabu ndi Ahagiri,
7 Agebala, Aamoni ndi Aamaleki,
Afilisti, pamodzi ndi anthu a ku Turo.
8 Ngakhalenso Aasiriya aphatikizana nawo
kupereka mphamvu kwa ana a Loti.

Sela

9 Muwachitire zomwe munachitira Amidiyani,
monga munachitira Sisera ndi Yabini ku mtsinje wa Kisoni.
10 Amene anawonongedwa ku Endori
ndi kukhala ngati zinyalala.
11 Anthu awo otchuka muwachite zomwe munachita Orebu ndi Zeebu
ana a mafumu muwachite zomwe munachita Zeba ndi Zalimuna,
12 amene anati, "Tiyeni tilande dziko
la msipu la Mulungu."

13 Muwasandutse fumbi lowuluka, Inu Mulungu wanga,
ngati mankhusu owuluka ndi mphepo.
14 Monga moto umatentha nkhalango,
kapena malawi a moto kuyatsa phiri,
15 kotero muwathamangitse ndi mphepo yamkuntho,
ndi kuwachititsa mantha ndi namondwe.
16 Muphimbe nkhope zawo ndi manyazi
kuti adzafunefune dzina lanu Yehova.

17 Achite manyazi ndi mantha nthawi zonse;
awonongeke mwa manyazi.
18 Adziwe kuti Inu amene dzina lanu ndi Yehova,
ndinu nokha Wammwambamwamba pa dziko lonse lapansi.

# Salimo 84

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a Gititi. Salimo la ana a Kora.

1 Malo anu okhalamo ndi okomadi,
Inu Yehova Wamphamvuzonse!
2 Moyo wanga ukulakalaka, mpaka kukomoka,
kufuna mabwalo a Yehova;
Mtima wanga ndi thupi langa zikufuwulira
Mulungu wamoyo.

3 Ngakhale timba wapeza nyumba yokhalamo,
ndiponso namzeze wadzipezera yekha chisa,
kumene amagonekako ana ake
pafupi ndi guwa lanu la nsembe,
Inu Yehova Wamphamvuzonse, Mfumu yanga ndi Mulungu wanga.
4 Odala amene amakhala m'Nyumba yanu;
nthawi zonse amakutamandani.
Sela

5 Odala amene mphamvu yawo ili mwa Inu,
mitima yawo ikufunitsitsa kuyenda m'misewu yopita ku Ziyoni.
6 Pamene akudutsa chigwa cha Baka,
amachisandutsa malo a akasupe;
mvula ya chizimalupsa imadzazanso mayiwe ake.
7 Iwo amanka nakulirakulira mphamvu
mpaka aliyense ataonekera pamaso pa Mulungu mu Ziyoni.

8 Imvani pemphero langa, Inu Yehova Mulungu Wamphamvuzonse;
mvereni Inu Mulungu wa Yakobo.
Sela
9 Yang'anani chishango chathu, Inu Mulungu;
yang'anani mokoma mtima pa wodzozedwa wanu.

10 N'kwabwino kukhala m'mabwalo anu tsiku limodzi
kuposa kukhala kwina kwake kwa zaka 1,000;
Ine ndingakonde kukhala mlonda wa pa khomo la Nyumba ya Mulungu wanga
kuposa kukhala m'matenti a anthu oyipa.
11 Pakuti Yehova Mulungu ndi dzuwa ndi chishango;
Yehova amapereka chisomo ndi ulemu;
Iye sawamana zinthu zabwino
iwo amene amayenda mwangwiro.

12 Inu Yehova Wamphamvuzonse,
wodala ndi munthu amene amakhulupirira Inu.

# Salimo 85

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la ana a Kora.

1 Yehova munakomera mtima dziko lanu;
munabwezeretsa ulemerero wa Yakobo.
2 Munakhululukira mphulupulu za anthu anu
ndi kuphimba machimo awo onse.

Sela

3 Munayika pambali ukali wanu wonse
ndi kutembenuka kuchoka ku mkwiyo wanu woopsa.

4 Tibwezeretseninso mwakale Inu Mulungu Mpulumutsi wathu,
ndipo mutichotsere mkwiyo wanu.
5 Kodi mudzatikwiyira mpaka liti?
Kodi mudzapitiriza kukwiya pa mibado yathu yonse?
6 Kodi simudzatitsitsimutsanso,
kuti anthu anu asangalale mwa Inu?
7 Tionetseni chikondi chanu chosatha, Inu Yehova,
ndipo tipatseni chipulumutso chanu.

8 Ndidzamvetsera zimene Yehova Mulungu adzanena;
Iye amalonjeza mtendere kwa anthu ake, oyera mtima ake,
koma musawalole kuti abwerere ku zopusa.
9 Ndithu chipulumutso chake chili pafupi ndi iwo amene amaopa Iye,
kuti ulemerero wake ukhale m'dziko lathu.

10 Chikondi ndi kukhulupirika zimakumana pamodzi;
chilungamo ndi mtendere zimapsompsonana.
11 Kukhulupirika kumatumphuka kuchokera ku dziko lapansi,
ndipo chilungamo chimayang'ana pansi kuchokera kumwamba.
12 Ndithu Yehova adzapereka chimene chili chabwino,
ndipo dziko lathu lidzapereka zokolola zake.
13 Wolungama amapita patsogolo pake
ndi kukonza njira za mapazi ake.

# Salimo 86

Pemphero la Davide.
1 Ndimvereni Yehova ndipo mundiyankhe,
pakuti ndine wosauka ndi wosowa.
2 Yang'anirani moyo wanga, pakuti ndine wodzipereka kwa Inu.
Inu ndinu Mulungu wanga;
pulumutsani mtumiki wanu amene amadalira Inu.
Inu ndinu Mulungu wanga.
3 Mundichitire chifundo, Inu Ambuye,
pakuti ndikuyitana Inu tsiku lonse.
4 Bweretsani chimwemwe kwa mtumiki wanu, Ambuye,
pakuti ndimadalira Inu.

5 Inu Ambuye, ndinu wokhululuka ndi wabwino,
wodzaza ndi chikondi kwa onse amene amayitana Inu.
6 Yehova imvani pemphero langa;
mvetserani kulira kwanga kofuna chifundo.
7 Pa tsiku la mavuto anga ndidzayitana Inu,
pakuti Inu mudzandiyankha.

8 Pakati pa milungu palibe wina wofanana nanu Ambuye;
palibe ntchito zolingana ndi ntchito zanu.
9 Mitundu yonse ya anthu imene munayipanga
idzabwera ndi kudzalambira pamaso panu Ambuye;

iwo adzabweretsa ulemerero pa dzina lanu.
10 Pakuti ndinu wamkulu ndipo mumachita zodabwitsa;
Inu nokha ndiye Mulungu.

11 Ndiphunzitseni njira yanu Yehova,
ndipo ndidzayenda m'choonadi chanu;
patseni mtima wosagawikana
kuti ndilemekeze dzina lanu.
12 Ndidzakutamandani Ambuye Mulungu wanga, ndi mtima wanga wonse;
ndidzalemekeza dzina lanu kwamuyaya.
13 Pakuti chikondi chanu n'chachikulu kwa ine;
mwandipulumutsa ku malo ozama a manda.

14 Inu Mulungu wanga, anthu odzikuza akundithira nkhondo;
anthu ankhanza akufuna kundipha,
amene salabadira za Inu.
15 Koma Ambuye ndinu Mulungu wachifundo ndi wokoma mtima,
wosakwiya msanga, wodzaza ndi chikondi ndi wokhulupirika.
16 Tembenukirani kwa ine ndipo ndichitireni chifundo;
perekani mphamvu zanu kwa mtumiki wanu
ndipo pulumutsani mwana wa mdzakazi wanu.
17 Mundionetse chizindikiro cha ubwino wanu
kuti adani achione ndi kuchititsidwa manyazi,
pakuti Yehova mwandithandiza ndi kunditonthoza.

# Salimo 87

Salimo la Ana a Kora.
1 Iye wakhazikitsa maziko ake pa phiri loyera;
2 Yehova amakonda zipata za Ziyoni
kupambana malo onse okhalamo a Yakobo.
3 Za ulemerero wako zimakambidwa,
Iwe mzinda wa Mulungu:
Sela
4 "Ndidzanena za Rahabe ndi Babuloni
pakati pa iwo amene amandidziwa.
Dzikonso la Filisitiya, Turo pamodzi ndi Kusi,
ndipo ndidzati, 'Uyu anabadwira m'Ziyoni.' "

5 Ndithudi, za Ziyoni adzanena kuti,
"Uyu ndi uyo anabadwira mwa iye,
ndipo Wammwambamwamba adzakhazikitsa iyeyo."
6 Yehova adzalemba m'buku la kawundula wa anthu a mitundu ina:
"Uyu anabadwira m'Ziyoni."
Sela
7 Oyimba ndi ovina omwe adzati,
"Akasupe anga onse ali mwa iwe."

# Salimo 88

Salimo la ana a Kora. Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Potsata mayimbidwe a nyimbo yoti: "Pa Matenda ndi pa Mazunzo." Ndakatulo ya Hemani, wa banja la Ezara.
1 Inu Yehova, Mulungu amene mumandipulumutsa,

usana ndi usiku ndimalira pamaso panu.
2 Pemphero langa lifike pamaso panu;
tcherani khutu lanu kuti mumve kulira kwanga.

3 Pakuti ndili ndi mavuto ambiri
ndipo moyo wanga ukuyandikira ku manda.
4 Ndikuwerengedwa pamodzi ndi iwo amene akutsikira ku dzenje;
ndine munthu wopanda mphamvu.
5 Ndayikidwa pambali pamodzi ndi anthu akufa,
monga ophedwa amene agona m'manda,
amene Inu simuwakumbukiranso,
amene achotsedwa pa chisamaliro chanu.

6 Mwandiyika pansi pa dzenje penipeni,
m'malo akuya a mdima waukulu.
7 Ukali wanu ukundipsinja kwambiri,
mwandiopseza kwambiri ndi mafunde anu onse.
Sela
8 Mwandichotsa pakati pa abwenzi anga enieni
ndipo mwachititsa kuti ndikhale chonyansa kwa iwo.
Ndatsekerezedwa ndipo sindingathe kuthawa;
9 maso anga ada ndi chisoni.

Ndimayitana Inu Yehova tsiku lililonse;
ndimakweza manja anga kwa Inu.
10 Kodi mumaonetsa zozizwitsa zanu kwa anthu akufa?
Kodi iwo amene afa amaukanso ndi kutamanda Inu?
Sela
11 Kodi chikondi chanu chimalalikidwa m'manda,
za kukhulupirika kwanu ku malo a chiwonongeko?
12 Kodi zozizwitsa zanu zimadziwika ku malo a mdima,
kapena ntchito zanu zolungama ku dziko la anthu oyiwalika?

13 Inu Yehova, Ine ndimalirira thandizo;
mmawa mapemphero anga amafika pamaso panu.
14 Inu Yehova n'chifukwa chiyani mukundikana
ndi kundibisira nkhope yanu?

15 Kuyambira ubwana wanga ndakhala ndikuzunzika pafupi kufa;
ndakhala ndikuchita mantha ndipo ndine wothedwa nzeru.
16 Ukali wanu wandimiza;
zoopsa zanu zandiwononga.
17 Tsiku lonse zimandizungulira ngati chigumula;
zandimiza kwathunthu.
18 Inu mwatenga anzanga ndi okondedwa anga kuwachotsa pamaso panga;
mdima ndiye bwenzi langa lenileni.

# Salimo 89

Ndakatulo ya Etani, wa banja la Ezara.
1 Ndidzayimba za chikondi chachikulu cha Yehova kwamuyaya;

ndi pakamwa panga ndidzachititsa kuti kukhulupirika kwanu kudziwike ku mibado yonse.
2 Ndidzalalikira kuti chikondi chanu chidzakhazikika mpaka muyaya,
kuti Inu munakhazikitsa kukhulupirika kwanu kumwamba kwenikweniko.

3 Inu munati, “Ndachita pangano ndi wosankhidwa wanga,
ndalumbira kwa Davide mtumiki wanga kuti,
4 ‘Ndidzakhazikitsa zidzukulu zako mpaka muyaya.
Ndidzachititsa kuti mpando wako waufumu ukhazikike ku mibado yonse,’ ”
Sela.

5 Mayiko akumwamba amatamanda zozizwitsa zanu Yehova,
kukhulupirika kwanunso, mu msonkhano wa oyera mtima anu.
6 Pakuti ndani mu mlengalenga angalingane ndi Yehova?
Ndani wofanana ndi Yehova pakati pa zolengedwa zakumwamba?
7 Mu msonkhano wa oyera mtima Mulungu amaopedwa kwambiri;
Iye ndiye wochititsa mantha kupambana onse amene amuzungulira.
8 Inu Yehova Mulungu Wamphamvuzonse, ndani wofanana nanu?
Yehova ndinu wamphamvu ndipo kukhulupirika kwanu kwakuzungulirani.

9 Mumalamula nyanja ya mafunde awukali;
pamene mafunde ake awundana Inu mumawakhalitsa bata.
10 Munaphwanya Rahabe monga munthu wophedwa;
ndi dzanja lanu lamphamvu munabalalitsa adani anu.
11 Mayiko akumwamba ndi anu ndiponso dziko lapansi ndi lanu;
munapanga dziko lonse ndi zonse zili m’menemo.
12 Munalenga Kumpoto ndi Kummwera;
Tabori ndi Herimoni akuyimba ndi chimwemwe pa dzina lanu.
13 Mkono wanu ndi wamphamvu;
dzanja lanu ndi lamphamvu, dzanja lanu lamanja ndi lopambana.

14 Chilungamo ndi chiweruzo cholungama ndiye maziko a mpando wanu waufumu;
chikondi ndi kukhulupirika zimayenda patsogolo panu.
15 Ndi odala amene aphunzira kuyamika Inu,
amene amayenda m’kuwunika kwa nkhope yanu Yehova.
16 Amakondwera m’dzina lanu tsiku lonse lathunthu;
amasangalala koposa m’chilungamo chanu.
17 Pakuti Inu ndiye ulemerero wawo ndi mphamvu yawo
ndipo mwa kukoma mtima kwanu Inu mumakweza nyanga yathu.
18 Ndithudi, chishango chathu ndi cha Yehova,
Mfumu yathu kwa Woyerayo wa Israeli.

19 Kale munayankhula m’masomphenya,
kwa anthu anu okhulupirika munati,
“Ndapatsa mphamvu wankhondo;
ndakweza mnyamata wochokera pakati pa anthu.
20 Ndamupeza mtumiki wanga Davide;

ndamudzoza ndi mafuta opatulika.
21 Dzanja langa lidzamuchirikiza;
zoonadi, mkono wanga udzamupatsa mphamvu.
22 Adani sadzamulamula kuti apereke msonkho;
anthu oyipa sadzamusautsa.
23 Ndidzaphwanya adani ake pamaso pake
ndi kukantha otsutsana naye.
24 Chikondi changa chokhulupirika chidzakhala naye,
ndipo kudzera m'dzina langa nyanga yake idzakwezedwa.
25 Ndidzayika dzanja lake pa nyanja,
dzanja lake lamanja pa mitsinje.
26 Iyeyo adzafuwula kwa Ine kuti, 'Ndinu Atate anga,
Mulungu wanga, Thanthwe ndi Chipulumutso changa.'
27 Ndidzamuyika kuti akhale mwana wanga woyamba kubadwa;
wokwezedwa kwambiri pakati pa mafumu a dziko lapansi.
28 Ndidzamusungira chifundo changa kwamuyaya,
ndipo pangano langa ndi iye silidzatha.
29 Ine ndidzakhazikitsa zidzukulu zake mpaka muyaya,
mpando wake waufumu ngati masiku a miyamba.

30 "Ngati ana ake adzataya lamulo langa
ndi kusatsatira malangizo anga,
31 ngati adzaswa malamulo anga
ndi kulephera kusunga ziphunzitso zanga,
32 Ine ndidzalanga tchimo lawo ndi ndodo,
mphulupulu zawo powakwapula.
33 Koma sindidzachotsa chikondi changa pa iye,
kapena kukhala wosakhulupirika kwa iyeyo.
34 Sindidzaswa pangano langa
kapena kusintha zimene milomo yanga yayankhula.
35 Ndinalumbira kamodzi mwa kuyera kwanga
ndipo sindidzanama kwa Davide,
36 kuti zidzukulu zake zidzakhale kwamuyaya
ndipo mpando wake waufumu udzakhazikika pamaso panga ngati dzuwa;
37 udzakhazikika kwamuyaya monga mwezi,
mboni yokhulupirika m'mitambo.

Sela

38 "Koma tsopano Inu mwamukana, mwamutaya,
mwamukwiyira kwambiri wodzozedwa wanu.
39 Mwakana pangano ndi mtumiki wanu
ndipo mwadetsa m'fumbi chipewa chake chaufumu.
40 Inu mwagumula makoma ake onse
ndipo mwasandutsa bwinja malinga ake.
41 Onse amene amadutsa amalanda zinthu zake;
iye wakhala chotonzedwa cha anansi ake.
42 Mwakweza dzanja lamanja la adani ake;
mwachititsa kuti adani ake akondwere.
43 Mwabunthitsa lupanga lake,
simunamuthandize pa nkhondo.

44 Inu mwathetsa kukongola kwa ulemerero wake
ndipo mwagwetsa pansi mpando wake waufumu.
45 Mwachepetsa masiku a unyamata wake;
mwamuphimba ndi chofunda chochititsa manyazi.
Sela

46 “Mpaka liti Yehova? Kodi mudzadzibisa mpaka kalekale?
Mpaka liti ukali wanu udzayaka ngati moto?
47 Kumbukirani kuti masiku a moyo wanga ndi ochepa
pakuti munalenga kwachabe anthu onse!
48 Kodi ndi munthu uti angakhale ndi moyo ndi kusaona imfa?
Kapena kudzipulumutsa yekha ku mphamvu ya manda?
Sela
49 Inu Ambuye kodi chili kuti chikondi chanu chachikulu choyamba chija,
chimene mwa kukhulupirika kwanu munalumbira kwa Davide?
50 Kumbukirani, Ambuye momwe mtumiki wanu wanyozedwera,
momwe ndakhalira ndi kusunga mu mtima mwanga mawu a pangano a anthu a mitundu yonse,
51 mawu achipongwe amene adani anu akhala akunyoza, Inu Yehova,
ndi mawu amene akhala akunyoza mayendedwe onse a wodzozedwa wanu.

52 “Matamando akhale kwa Yehova mpaka muyaya!”
Ameni ndi Ameni.

# BUKU LACHINAYI

## 90

*Masalimo 90–106*

Pemphero la Mose munthu wa Mulungu.
1 Ambuye, mwakhala muli malo athu okhalamo
pa mibado yonse.
2 Mapiri asanabadwe,
musanalenge n’komwe dziko lapansi ndi dziko lonse,
kuyambira muyaya mpaka muyaya Inu ndinu Mulungu.

3 Inu mumabwezera anthu ku fumbi,
mumati, “Bwerera ku fumbi iwe mwana wa munthu.”
4 Pakuti zaka 1,000 pamaso panu
zili ngati tsiku limene lapita
kapena ngati kamphindi ka usiku.
5 Inu mumasesa anthu m’tulo ta imfa,
iwo ali ngati udzu watsopano wa mmawa,
6 ngakhale kuti mmawa umaphuka watsopano,
pofika madzulo wauma ndi kufota.

7 Ife tathedwa ndi mkwiyo wanu;
ndipo taopsezedwa ndi kuyipidwa kwanu.
8 Mwayika mphulupulu zathu pamaso panu,
machimo athu obisika poonekera pamaso panu.
9 Masiku athu onse amatha ali pansi pa ukali wanu;
timatsiriza zaka zathu ndi kubuwula.
10 Kuchuluka kwa masiku athu ndi 70,

kapena 80 ngati tili ndi mphamvu;
komabe zaka zonsezi ndi za mavuto ndi nkhawa,
zimatha mofulumira ndipo ife timawulukira kutali.

11 Kodi ndani amadziwa mphamvu ya mkwiyo wanu?
Pakuti ukali wanu ndi waukulu ngati ulemu umene uyenera Inu.
12 Tiphunzitseni kuwerenga masiku athu molondola,
kuti tikhale ndi mtima wanzeru.

13 Lezani mtima Inu Yehova! Kodi mudzatikwiyira mpaka liti?
Achitireni chifundo atumiki anu.
14 Mutikhutitse mmawa ndi chikondi chanu chosatha,
kuti tiyimbe ndi chimwemwe ndi kukhala okondwa masiku athu onse.
15 Tisangalatseni masiku ambiri monga masiku amene mwatisautsa,
kwa zaka zambiri monga momwe tinaonera mavuto.
16 Ntchito zanu zionetsedwe kwa atumiki anu,
kukongola kwanu kwa ana awo.

17 Kukoma mtima kwa Ambuye Mulungu wathu kukhale pa ife;
tikhazikitsireni ntchito ya manja athu;
inde, khazikitsani ntchito ya manja athu.

# Salimo 91

1 Iye amene amakhala mu mthunzi wa Wammwambamwamba
adzapuma mu mthunzi wa Wamphamvuzonse.
2 Ndidzanena za Yehova, "Iye ndiye pothawira panga ndi linga langa,
Mulungu wanga amene ndimadalira."

3 Ndithu, Iye adzakupulumutsa ku msampha wa mlenje
ndi ku mliri woopsa;
4 Adzakuphimba ndi nthenga zake,
ndipo udzapeza malo othawira m'mapikomo;
kukhulupirika kwake kudzakhala chishango chako ndi lihawo.
5 Sudzachita mantha ndi zoopsa za usiku,
kapena muvi wowuluka masana,
6 kapena mliri umene umayenda mu mdima,
kapena zowononga za pa nthawi ya masana.
7 Anthu 1,000 atha kufa pambali pako,
anthu 10,000 kudzanja lako lamanja,
koma zoopsazo sizidzafika pafupi ndi iwe.
8 Udzapenya ndi maso ako
ndipo udzaona mmene anthu oyipa amalangidwira.

9 Pakuti wasankha Wammwambamwamba kukhala malo ako okhalamo;
wavomera Yehova kukhala kothawira kwako.
10 Choncho palibe choyipa chimene chidzakugwera,
zoopsa sizidzafika pafupi ndi tenti yako.
11 Pakuti adzalamulira angelo ake za iwe,
kuti akutchinjirize mosamala pa njira zako zonse;
12 ndipo adzakunyamula ndi manja awo,
kuti phazi lako lisagunde pa mwala.
13 Udzapondaponda mkango ndi njoka,

udzapondereza mkango wamphamvu ndiponso chinjoka.

14 “Chifukwa iye amandikonda,” akutero Yehova, “Ndidzamulanditsa;
ndidzamuteteza pakuti wavomereza dzina langa.
15 Adzandiyitana, ndipo ndidzamuyankha;
ndidzakhala naye pa mavuto,
ndidzamupulumutsa ndi kumulemekeza.
16 Ndidzamupatsa moyo wautali
ndi kumupulumutsa.”

# Salimo 92

Salimo. Nyimbo ya pa tsiku la Sabata.
1 N’kwabwino kutamanda Yehova
ndi kuyimbira nyimbo dzina lanu, Inu Wammwambamwamba,
2 Kulengeza chikondi chanu mmawa,
ndi kukhulupirika kwanu nthawi ya usiku,
3 kuyimbira nyimbo choyimbira cha zingwe khumi
ndi mayimbidwe abwino a zeze.

4 Pakuti Inu mumandisangalatsa ndi ntchito zanu, Inu Yehova;
Ine ndikuyimba mwachimwemwe pa ntchito ya manja anu.
5 Ndi yayikuludi ntchito yanu Yehova,
maganizo anu ndi ozamadi!
6 Munthu wopanda nzeru sadziwa,
zitsiru sizizindikira,
7 kuti ngakhale anthu oyipa aphuka ngati udzu
ndipo anthu onse ochita zoyipa apindula,
adzawonongedwa kwamuyaya.

8 Koma Inu Yehova, ndinu wokwezedwa kwamuyaya.

9 Zoonadi adani anu Yehova,
zoonadi adani anu adzawonongeka;
onse ochita zoyipa adzabalalitsidwa.
10 Inu mwakweza nyanga yanga ngati nyanga ya njati;
mafuta abwino akhuthulidwa pamutu wanga.
11 Maso anga aona kugonjetsedwa kwa olimbana nane,
makutu anga amva za kugwa kwa amaliwongo anga oyipa.

12 Anthu olungama adzaphuka ngati mtengo wa mgwalangwa,
adzakula ngati mkungudza wa ku Lebanoni;
13 odzalidwa m’nyumba ya Yehova,
adzakula bwino m’mabwalo a Mulungu wathu.
14 Iwo adzaberekabe zipatso mu ukalamba wawo,
adzakhala anthete ndi obiriwira,
15 kulengeza kuti, “Yehova ndi wolungama;
Iye ndiye Thanthwe langa, ndipo mwa Iye mulibe choyipa.”

# Salimo 93

1 Yehova akulamulira, wavala ulemerero;
Yehova wavala ulemerero ndipo wadzimangirira mphamvu,
dziko lonse lakhazikika kolimba; silingasunthidwe.

2 Mpando wanu waufumu unakhazikika kalekale;
Inu ndinu wamuyaya.

3 Nyanja zakweza Inu Yehova,
nyanja zakweza mawu ake;
nyanja zakweza mafunde ake ochita mkokomo.
4 Yehova ndi wamphamvu kupambana mkokomo wa madzi ambiri,
ndi wamphamvu kupambana mafunde a nyanja,
Yehova mmwamba ndi wamphamvu.

5 Malamulo anu Yehova ndi osasinthika;
chiyero chimakongoletsa nyumba yanu
mpaka muyaya.

# Salimo 94

1 Inu Yehova, ndinu Mulungu wobwezera chilango,
Inu Mulungu amene mumabwezera chilango, wonetsani kuwala kwanu.
2 Nyamukani, Inu woweruza wa dziko lapansi;
bwezerani kwa odzikuza zowayenera.
3 Kodi mpaka liti anthu oyipa Inu Yehova,
mpaka liti anthu oyipa adzalumpha ndi chimwemwe?

4 Amakhuthula mawu onyada;
onse ochita zoyipa ndi odzaza ndi kudzikuza.
5 Amaphwanya anthu anu, Inu Yehova;
amapondereza cholowa chanu.
6 Amaphanso amayi a masiye ndi alendo okhala nawo m'dziko;
amapha ana amasiye.
7 Iwo amati, "Yehova sakuona;
Mulungu wa Yakobo salabadirako."

8 Samalani, inu anthu opanda nzeru pakati pa anthu;
zitsiru inu, kodi mudzakhala liti anzeru?
9 Kodi Iye amene anapanga khutu sangathe kumva?
Kodi Iye amene anapanga diso sangathe kuona?
10 Kodi Iye amene amalangiza mitundu ya anthu sangathenso kulanga?
Kodi Iye amene amaphunzitsa munthu angasowe nzeru?
11 Yehova amadziwa maganizo a munthu;
Iye amadziwa kuti maganizowo ndi achabechabe.

12 Wodala munthu amene Inu Yehova mumamulangiza,
munthu amene mumamuphunzitsa kuchokera mulamulo lanu;
13 mumamupumitsa pa nthawi ya mavuto,
mpaka woyipa atakumbiridwa dzenje.
14 Pakuti Yehova sadzawakana anthu ake;
Iye sadzasiya cholowa chake.
15 Chiweruzo chidzakhazikikanso pa chilungamo,
ndipo onse olungama mtima adzachitsata.

16 Ndani adzadzuka chifukwa cha ine kulimbana ndi anthu oyipa?

Ndani adzayimirira m’malo mwanga kulimbana ndi anthu ochita zoyipa?
17 Yehova akanapanda kundithandiza,
bwenzi nditakakhala msanga ku malo achete a imfa.
18 Ndikanena kuti, “Phazi langa likuterereka,”
chikondi chanu, Inu Yehova, chimandichirikiza.
19 Pamene nkhawa inakula m’kati mwanga,
chitonthozo chanu chinabweretsa chimwemwe m’moyo mwanga.

20 Kodi mpando waufumu woyipa ungathe kugwirizana nanu
umene umabweretsa masautso chifukwa cha malamulo ake?
21 Iwo amasonkhana pamodzi kulimbana ndi wolungama
ndi kugamula kuti wosalakwa aphedwe.
22 Koma Yehova wakhala linga langa,
ndipo Mulungu ndiye thanthwe limene ndimathawirako.
23 Iye adzawabwezera chifukwa cha machimo awo
ndi kuwawononga chifukwa cha kuyipa kwawo;
Yehova Mulungu wathu adzawawononga.

# Salimo 95

1 Bwerani, tiyeni timuyimbire Yehova mwachimwemwe,
tiyeni tifuwule kwa Thanthwe la chipulumutso chathu
2 Tiyeni tibwere pamaso pake ndi chiyamiko
ndipo mupembedzeni Iyeyo ndi zida zoyimbira ndi nyimbo.

3 Pakuti Yehova ndi Mulungu wamkulu,
mfumu yayikulu pamwamba pa milungu yonse.
4 M’manja mwake muli maziko ozama a dziko lapansi,
ndipo msonga za mapiri ndi zake.
5 Nyanja ndi yake, pakuti anayilenga ndi Iye,
ndipo manja ake anawumba mtunda wowuma.

6 Bwerani, tiyeni tiwerame pomulambira,
tiyeni tigwade pamaso pa Yehova Mlengi wathu;
7 pakuti Iye ndiye Mulungu wathu
ndipo ife ndife anthu a pabusa pake,
ndi nkhosa za m’dzanja lake.

Lero ngati inu mumva mawu ake,
8 musawumitse mitima yanu monga momwe munachitira pa Meriba,
monga munachitira tsiku lija pa Masa m’chipululu.
9 Kumene makolo anu anandiyesa ndi kundiputa,
ngakhale anaona zimene Ine ndinazichita.
10 Kwa zaka makumi anayi ndinali wokwiya ndi m’bado umenewo;
ndipo ndinati, “Iwo ndi anthu amene mitima yawo imasochera
ndipo sanadziwe njira zanga.”
11 Choncho ndili chikwiyire, ndinalumbira kuti,
“Iwowa sadzalowa ku malo anga a mpumulo.”

# Salimo 96

1 Imbirani Yehova nyimbo yatsopano;

Imbirani Yehova dziko lonse lapansi.
2 Imbirani Yehova, tamandani dzina lake;
lalikirani chipulumutso chake tsiku ndi tsiku.
3 Lengezani ulemerero wake pakati pa mayiko,
ntchito zake zodabwitsa pakati pa mitundu yonse ya anthu.

4 Pakuti wamkulu ndi Yehova ndipo ndi woyenera kwambiri kumutamanda;
ayenera kuopedwa kupambana milungu yonse.
5 Pakuti milungu yonse ya anthu a mitundu ina ndi mafano,
koma Yehova analenga mayiko akumwamba.
6 Ulemu ndi ufumu zili pamaso pake,
mphamvu ndi ulemerero zili m'malo ake opatulika.

7 Perekani kwa Yehova, inu mabanja a anthu a mitundu ina,
perekani kwa Yehova ulemerero ndi mphamvu.
8 Perekani kwa Yehova ulemerero woyenera dzina lake;
bweretsani chopereka ndipo mulowe m'mabwalo ake.
9 Lambirani Yehova mu ulemerero wa chiyero chake;
njenjemerani pamaso pake, dziko lonse lapansi.

10 Nenani pakati pa mitundu ya anthu, "Yehova akulamulira."
Dziko lonse lakhazikika molimba, silingasunthidwe;
Iye adzaweruza mitundu ya anthu molungama.
11 Mayiko akumwamba asangalale, dziko lapansi likondwere;
nyanja ikokome, ndi zonse zili m'menemo;
12 minda ikondwere pamodzi ndi chilichonse chili m'menemo.
Pamenepo mitengo yonse ya m'nkhalango idzayimba ndi chimwemwe;
13 idzayimba pamaso pa Yehova,
pakuti Iye akubwera kudzaweruza dziko lapansi;
adzaweruza dziko lonse mwachilungamo
ndi mitundu ya anthu onse m'choonadi.

# Salimo 97

1 Yehova akulamulira, dziko lapansi lisangalale;
magombe akutali akondwere.

2 Mitambo ndi mdima waukulu zamuzungulira;
chilungamo ndi kuweruza molungama ndiwo maziko a mpando wake waufumu.
3 Moto umapita patsogolo pake
ndi kunyeketsa amaliwongo kumbali zonse.
4 Zing'aning'ani zake zimawalitsa dziko lonse;
dziko lapansi limaona ndipo limanjenjemera.
5 Mapiri amasungunuka ngati phula pamaso pa Yehova,
pamaso pa Ambuye a dziko lonse lapansi.
6 Mayiko akumwamba amalengeza za chilungamo chake,
ndipo mitundu yonse ya anthu imaona ulemerero wake.

7 Onse amene amalambira mafano osema amachititsidwa manyazi,
iwo amene amanyadira mafano;
mulambireni, inu milungu yonse!

8 Ziyoni akumva ndipo akukondwera,
midzi ya Yuda ikusangalala
chifukwa cha maweruzo anu Yehova.
9 Pakuti Inu Yehova ndi Wammwambamwamba pa dziko lonse lapansi;
ndinu wokwezeka kupambana milungu yonse.

10 Iwo amene amakonda Yehova adane ndi zoyipa
pakuti Iye amayang'anira miyoyo ya amene amamukhulupirira
ndipo amawapulumutsa m'dzanja la anthu oyipa
11 Kuwala kumafika pa anthu olungama,
ndi chimwemwe kwa olungama mtima.
12 Kondwerani mwa Yehova Inu olungama
ndipo tamandani dzina lake loyera.

# Salimo 98

Salimo.
1 Imbirani Yehova nyimbo yatsopano,
pakuti Iyeyo wachita zinthu zodabwitsa;
dzanja lake lamanja ndi mkono wake woyera
zamuchitira chipulumutso.
2 Yehova waonetsa chipulumutso chake
ndipo waulula chilungamo chake kwa anthu a mitundu ina.
3 Iye wakumbukira chikondi chake
ndi kukhulupirika kwake pa Aisraeli;
malekezero onse a dziko lapansi aona
chipulumutso cha Mulungu wathu.

4 Fuwulani mwachimwemwe kwa Yehova, dziko lonse lapansi,
muyimbireni nyimbo mofuwula ndi mokondwera.
5 Imbirani Yehova nyimbo ndi zeze,
ndi zeze ndi mawu a kuyimba,
6 ndi malipenga ndi kuliza kwa nyanga ya nkhosa yayimuna
fuwulani mwachimwemwe pamaso pa Yehova Mfumu.

7 Nyanja ikokome pamodzi ndi zonse zili m'menemo,
dziko lonse ndi onse amene amakhala m'menemo.
8 Mitsinje iwombe m'manja mwawo,
mapiri ayimbe pamodzi mwachimwemwe;
9 izo ziyimbe pamaso pa Yehova,
pakuti Iye akubwera kudzaweruza dziko lapansi.
Adzaweruza dziko lonse mwachilungamo,
ndi mitundu ya anthu mosakondera.

# Salimo 99

1 Yehova akulamulira,
mitundu ya anthu injenjemere;
Iye wakhala pa mpando wake waufumu, pakati pa akerubi,
dziko lapansi ligwedezeke.
2 M'ziyoni wamkulu ndi Yehova;
Iye ndi wokwezeka pamwamba pa mitundu yonse ya anthu.
3 Anthu atamande dzina lanu lalikulu ndi loopsa kwambiri,
Iye ndi woyera.

4 Mfumu yamphamvu, iyo imakonda chilungamo
Inu mwakhazikitsa khalidwe losakondera;
mwachita zolungama ndi zoyenera mwa Yakobo.
5 Kwezani Yehova Mulungu wathu
ndipo mulambireni pa mapazi ake;
Iye ndi woyera.

6 Mose ndi Aaroni anali ena mwa ansembe ake,
Samueli anali pamodzi ndi iwo amene anayitana pa dzina lake;
iwo anayitana Yehova
ndipo Iyeyo anawayankha.
7 Iye anayankhula nawo kuchokera m'chipilala cha mtambo;
iwo anasunga malamulo ake ndi zophunzitsa zomwe anawapatsa.

8 Inu Yehova Mulungu wathu,
munawayankha iwo;
Inu kwa Israeli munali Mulungu wokhululuka,
ngakhale munawalanga pa zochita zawo zoyipa.
9 Kwezani Yehova Mulungu wathu
ndipo mumulambire pa phiri lake loyera,
pakuti Yehova Mulungu wathu ndi woyera.

# Salimo 100

Salimo. Nyimbo yothokoza.
1 Fuwulani kwa Yehova mwachimwemwe, inu dziko lonse lapansi.
2 Mulambireni Yehova mosangalala;
bwerani pamaso pake ndi nyimbo zachikondwerero.
3 Dziwani kuti Yehova ndi Mulungu.
Iye ndiye amene anatipanga ndipo ife ndife ake;
ndife anthu ake, nkhosa za pabusa pake.

4 Lowani ku zipata zake ndi chiyamiko
ndi ku mabwalo ake ndi matamando;
muyamikeni ndi kutamanda dzina lake.
5 Pakuti Yehova ndi wabwino ndipo chikondi chake ndi chamuyaya;
kukhulupirika kwake n'kokhazikika pa mibado ndi mibado.

# Salimo 101

Salimo la Davide.
1 Ndidzayimba za chikondi ndi chiweruzo chanu cholungama;
kwa Inu Yehova ndidzayimba matamando.
2 Ndidzatsata njira yolungama;
nanga mudzabwera liti kwa ine?

Ndidzayenda m'nyumba mwanga
ndi mtima wosalakwa.
3 Sindidzayika chinthu chilichonse choyipa
pamaso panga.

Ine ndimadana ndi zochita za anthu opanda chikhulupiriro;
iwo sadzadziphatika kwa ine.
4 Anthu a mtima wokhota adzakhala kutali ndi ine;

ine sindidzalola choyipa chilichonse kulowa mwa ine.

5 Aliyense wosinjirira mnansi wake mseri
ameneyo ndidzamuletsa;
aliyense amene ali ndi maso amwano ndi mtima wodzikuza,
ameneyo sindidzamulekerera.

6 Maso anga adzakhala pa okhulupirika m'dziko,
kuti akhale pamodzi ndi ine;
iye amene mayendedwe ake ndi wosalakwa
adzanditumikira.

7 Aliyense wochita chinyengo
sadzakhala m'nyumba mwanga.
Aliyense woyankhula mwachinyengo
sadzayima pamaso panga.

8 Mmawa uliwonse ndidzatontholetsa anthu
onse oyipa m'dziko;
ndidzachotsa aliyense wochita zoyipa
mu mzinda wa Yehova.

# Salimo 102

Pemphero la munthu wosautsidwa, pamene walefuka, nakhuthulira pamaso pa Yehova kulira kwakeko.

1 Yehova imvani pemphero langa;
kulira kwanga kopempha thandizo kufike kwa Inu.
2 Musandibisire nkhope yanu
pamene ndili pa msautso.
Munditcherere khutu;
pamene ndiyitana ndiyankheni msanga.

3 Pakuti masiku anga akupita ngati utsi;
mafupa anga akunyeka ngati nkhuni zoyaka.
4 Mtima wanga wakanthidwa ndipo ukufota ngati udzu;
ndipo ndimayiwala kudya chakudya changa.
5 Chifukwa cha kubuwula kwanga kofuwula
ndatsala chikopa ndi mafupa okhaokha.
6 Ndili ngati kadzidzi wa ku chipululu,
monga kadzidzi pakati pa mabwinja.
7 Ndimagona osapeza tulo; ndakhala
ngati mbalame yokhala yokha pa denga.
8 Tsiku lonse adani anga amandichita chipongwe;
iwo amene amandinyoza, amagwiritsa ntchito dzina langa ngati temberero.
9 Pakuti ndimadya phulusa ngati chakudya changa
ndi kusakaniza chakumwa changa ndi misozi
10 chifukwa cha ukali wanu waukulu,
popeza Inu mwandinyamula ndi kunditayira kumbali.
11 Masiku anga ali ngati mthunzi wa kumadzulo;
Ine ndikufota ngati udzu.

12 Koma Inu Yehova, muli pa mpando wanu waufumu kwamuyaya;
kudziwika kwanu ndi kokhazikika ku mibado yonse.
13 Inu mudzadzuka ndi kuchitira chifundo Ziyoni
pakuti ndi nthawi yoti muonetse kukoma mtima kwanu pa iyeyo;
nthawi yoyikika yafika.
14 Pakuti miyala yake ndi yokondedwa kwa atumiki anu;
fumbi lake lokha limawachititsa kuti amve chisoni.
15 Mitundu ya anthu idzaopa dzina la Yehova,
mafumu onse a dziko lapansi adzalemekeza ulemerero wanu.
16 Pakuti Yehova adzamanganso Ziyoni
ndi kuonekera mu ulemerero wake.
17 Iye adzayankha pemphero la anthu otayika;
sadzanyoza kupempha kwawo.

18 Zimenezi zilembedwe chifukwa cha mibado ya m'tsogolo,
kuti anthu amene sanabadwe adzatamande Yehova:
19 "Yehova anayang'ana pansi kuchokera ku malo ake opatulika mmwamba,
kuchokera kumwamba anayang'ana dziko lapansi,
20 kuti amve kubuwula kwa anthu a m'ndende,
kuti apulumutse amene anayenera kuphedwa."
21 Kotero dzina la Yehova lidzalengezedwa mu Ziyoni
ndi matamando ake mu Yerusalemu,
22 pamene mitundu ya anthu ndi maufumu
adzasonkhana kuti alambire Yehova.

23 Iye anathyola mphamvu zanga pa nthawi ya moyo wanga;
Iyeyo anafupikitsa masiku anga.
24 Choncho Ine ndinati:
"Musandichotse, Inu Mulungu wanga, pakati pa masiku a moyo wanga;
zaka zanu zimakhalabe pa mibado yonse.
25 Pachiyambi Inu munakhazikitsa maziko a dziko lapansi
ndipo mayiko akumwamba ndi ntchito ya manja anu.
26 Izi zidzatha, koma Inu mudzakhalapo;
zidzatha ngati chovala.
Mudzazisintha ngati chovala
ndipo zidzatayidwa.
27 Koma Inu simusintha,
ndipo zaka zanu sizidzatha.
28 Ana a atumiki anu adzakhala pamaso panu;
zidzukulu zawo zidzakhazikika pamaso panu."

# Salimo 103

Salimo la Davide.
1 Tamanda Yehova, iwe moyo wanga;
ndi zonse zam'kati mwanga zitamande dzina lake loyera.
2 Tamanda Yehova, iwe moyo wanga,
ndipo usayiwale zabwino zake zonse.
3 Amene amakhululuka machimo ako onse
ndi kuchiritsa nthenda zako zonse,
4 amene awombola moyo wako ku dzenje

ndi kukuveka chikondi ndi chifundo chake ngati chipewa chaufumu,
5 amene akwaniritsa zokhumba zako ndi zinthu zabwino,
kotero kuti umakhala wamphamvu zatsopano ngati mphungu.

6 Yehova amachita chilungamo
ndipo amaweruza molungama onse opsinjika.

7 Iye anadziwitsa Mose njira zake,
ntchito zake kwa Aisraeli.
8 Yehova ndi wachifundo ndi wokoma mtima,
wosakwiya msanga ndi wachikondi chochuluka.
9 Iye sadzatsutsa nthawi zonse,
kapena kusunga mkwiyo wake kwamuyaya;
10 satichitira molingana ndi machimo athu,
kapena kutibwezera molingana ndi mphulupulu zathu.
11 Pakuti monga kumwamba kuli kutali ndi dziko lapansi,
koteronso chikondi chake n'chachikulu kwa iwo amene amamuopa;
12 monga kummawa kutalikirana ndi kumadzulo,
koteronso Iye watichotsera mphulupulu zathu kuti zikhale kutali nafe.
13 Monga bambo amachitira chifundo ana ake,
choncho Yehova ali ndi chifundo ndi iwo amene amamuopa;
14 pakuti Iye amadziwa momwe tinawumbidwira,
amakumbukira kuti ndife fumbi.
15 Kunena za munthu, masiku ake ali ngati udzu,
amaphuka ngati duwa la m'munda;
16 koma mphepo imawombapo ndipo silionekanso
ndipo malo ake sakumbukirikanso.
17 Koma kuchokera muyaya mpaka muyaya
chikondi cha Yehova chili ndi iwo amene amamuopa,
ndi chilungamo chake chili ndi ana a ana awo;
18 iwo amene amasunga pangano lake
ndi kukumbukira kumvera malangizo ake.

19 Yehova wakhazikitsa mpando wake waufumu mmwamba
ndipo ufumu wake umalamulira onse.

20 Tamandani Yehova, inu angelo ake,
amphamvu inu amene mumachita zimene amalamula,
amene mumamvera mawu ake.
21 Tamandani Yehova, zolengedwa zonse zakumwamba,
inu atumiki ake amene mumachita chifuniro chake.
22 Tamandani Yehova, ntchito yake yonse
kulikonse mu ulamuliro wake.

Tamanda Yehova, iwe moyo wanga.

# Salimo 104

1 Tamanda Yehova, iwe moyo wanga.

Inu Yehova Mulungu wanga, ndinu wamkulu kwambiri;
mwavala ulemerero ndi ufumu.

2 Iye wadzifunditsa kuwala ngati chovala;
watambasula miyamba ngati tenti
3 ndipo wayika pa madzi mitanda ya chipinda chake.
Iye amasandutsa mitambo kukhala galeta lake,
ndi kuwuluka pa mapiko a mphepo.
4 Amapanga mphepo kukhala amithenga ake,
malawi amoto kukhala atumiki ake.

5 Anakhazikitsa dziko lapansi pa maziko ake;
silingasunthike.
6 Munaliphimba ndi nyanja yozama ngati chovala;
madzi anayimirira pamwamba pa mapiri.
7 Koma pakudzudzula kwanu madzi anathawa,
pa mkokomo wa bingu lanu iwo anamwazika;
8 Inu munamiza mapiri,
iwo anatsikira ku zigwa
kumalo kumene munawakonzera.
9 Inu munayika malire ndipo sangathe kudutsa,
iwo sadzamizanso dziko lapansi.

10 Iye achititsa akasupe kutulutsa madzi kupita ku zigwa;
madziwo amayenda pakati pa mapiri.
11 Iwo amapereka madzi kwa zirombo zonse zakuthengo;
abulu akuthengo amapha ludzu lawo.
12 Mbalame zamlengalenga zimayika zisa m’mbali mwa madzi;
zimayimba pakati pa thambo.
13 Iye amathirira mapiri kuchokera ku zipinda zake zapamwamba;
dziko lapansi limakhutitsidwa ndi chipatso cha ntchito yake.
14 Amameretsa udzu kuti ng’ombe zidye,
ndi zomera, kuti munthu azilima
kubweretsa chakudya kuchokera m’dziko lapansi:
15 vinyo amene amasangalatsa mtima wa munthu,
mafuta amene amachititsa nkhope yake kuwala,
ndi buledi amene amapereka mphamvu.
16 Mitengo ya Yehova ndi yothiriridwa bwino,
mikungudza ya ku Lebanoni imene Iye anadzala.
17 Mbalame zimamanga zisa zawo;
kakowa ali ndi malo ake m’mikungudzamo.
18 Mapiri ataliatali ndi a mbalale;
m’ming’alu ya miyala ndi mobisalamo mbira.

19 Mwezi umasiyanitsa nyengo
ndipo dzuwa limadziwa nthawi yake yolowera.
20 Inu mumabweretsa mdima nukhala usiku,
ndipo zirombo zonse za ku nkhalango zimatuluka.
21 Mikango imabangula kufuna nyama,
ndi kufunafuna chakudya chawo kuchokera kwa Mulungu.
22 Dzuwa limatuluka ndipo iyo imapita kukabisala;
imabwerera kukagona pansi m’mapanga awo.
23 Pamenepo munthu amapita ku ntchito yake,
kukagwira ntchito yake mpaka madzulo.

24 Ntchito zanu ndi zochulukadi Inu Yehova!
Munazipanga zonse mwanzeru,
dziko lapansi ladzaza ndi zolengedwa zanu.
25 Kuli nyanja yayikulu ndi yotambalala,
yodzaza ndi zolengedwa zosawerengeka,
zamoyo zanu zazikulu ndi zazing'ono zomwe.
26 Kumeneko sitima zapamadzi zimayenda uku ndi uku,
ndiponso Leviyatani amene munamulenga kuti asewere kumeneko.

27 Zonsezi zimayang'ana kwa Inu
kuti muzipatse chakudya chawo pa nthawi yake yoyenera.
28 Mukazipatsa,
zimachisonkhanitsa pamodzi;
mukatsekula dzanja lanu,
izo zimakhutitsidwa ndi zinthu zabwino.
29 Mukabisa nkhope yanu,
izo zimachita mantha aakulu;
mukachotsa mpweya wawo,
zimafa ndi kubwerera ku fumbi.
30 Mukatumiza mzimu wanu,
izo zimalengedwa
ndipo mumakozanso maonekedwe a dziko lapansi.

31 Ulemerero wa Yehova ukhalebe mpaka muyaya;
Yehova akondwere ndi ntchito ya manja ake;
32 Iye amene amayang'ana dziko lapansi ndipo limanjenjemera,
amene amakhudza mapiri ndipo amatuluka utsi.

33 Ine ndidzayimbira Yehova moyo wanga wonse;
ndidzayimbira matamando Mulungu wanga nthawi yonse imene ndili ndi moyo.
34 Zolingalira zanga zikhale zomukomera Iye,
pamene ndikusangalala mwa Yehova.
35 Koma anthu ochimwa awonongeke pa dziko lapansi
ndipo anthu oyipa asapezekenso.

Tamanda Yehova, Iwe moyo wanga.

Tamandani Yehova.

# Salimo 105

1 Yamikani Yehova, itanani dzina lake;
lalikirani pakati pa anthu a mitundu ina zimene Iye wachita.
2 Imbirani Iye, imbani matamando kwa Iyeyo;
fotokozani za machitidwe ake onse odabwitsa.
3 Munyadire dzina lake loyera;
mitima ya iwo amene amafunafuna Yehova ikondwere.
4 Dalirani Yehova ndi mphamvu zake;
funafunani nkhope yake nthawi yonse.

5 Kumbukirani zodabwitsa zimene Iye anazichita,
zozizwitsa zake ndi maweruzo amene anapereka,

6 inu zidzukulu za Abrahamu mtumiki wake,
inu ana a Yakobo, osankhika ake.
7 Iye ndiye Yehova Mulungu wathu;
maweruzo ake ali pa dziko lonse lapansi.

8 Iyeyo amakumbukira pangano lake kwamuyaya,
mawu amene analamula kwa mibado yonse,
9 pangano limene Iye anapanga ndi Abrahamu,
lumbiro limene analumbira kwa Isake.
10 Iye analitsimikiza kwa Yakobo monga zophunzitsa,
kwa Israeli monga pangano lamuyaya:
11 "Ndidzapereka kwa iwe dziko la Kanaani
ngati gawo la cholowa chako."

12 Pamene iwo anali ngati anthu ochepa m'chiwerengero,
ochepa ndithu, ndiponso alendo m'dzikolo,
13 ankayendayenda kuchoka ku mtundu wina wa anthu ndi kupita ku mtundu wina,
kuchoka mu ufumu wina kupita ku wina.
14 Iye sanalole wina aliyense kuwapondereza;
anadzudzula mafumu chifukwa cha iwo:
15 "Musakhudze odzozedwa anga;
musachitire choyipa aneneri anga."

16 Iye anabweretsa njala pa dziko
ndipo anawononga chakudya chonse;
17 Iyeyo anatumiza munthu patsogolo pawo,
Yosefe anagulitsidwa ngati kapolo.
18 Iwo anavulaza mapazi ake ndi matangadza,
khosi lake analiyika m'zitsulo,
19 mpaka zimene Iye ananeneratu zitakwaniritsidwa,
mpaka mawu a Yehova ataonetsa kuti Iye ananena zoona.
20 Mfumu inatuma munthu kukamumasula,
wolamulira wa mitundu ya anthu anamasula iyeyo.
21 Anamuyika kukhala wolamulira nyumba yake,
wolamulira zonse zimene iye anali nazo,
22 kulangiza ana a mfumu monga ankafunira
ndi kuphunzitsa nzeru akuluakulu.

23 Tsono Israeli analowa mu Igupto;
Yakobo anakhala monga mlendo m'dziko la Hamu.
24 Yehova anachulukitsa anthu ake;
ndipo anachititsa kuti akhale ochuluka kwambiri kuposa adani awo;
25 amene mitima yawo anayitembenuza kuti idane ndi anthu ake,
kukonzera chiwembu atumiki ake.
26 Yehova anatuma Mose mtumiki wake,
ndi Aaroni amene Iye anamusankha.
27 Iwo anachita zizindikiro zozizwitsa pakati pawo,
zodabwitsa zake m'dziko la Hamu.
28 Yehova anatumiza mdima nasandutsa dziko kuti likhale la mdima.
Koma anthuwo anakaniratu mawu a Yehova.
29 Yehova anasandutsa madzi awo kukhala magazi,

kuchititsa kuti nsomba zawo zife.
30 Dziko lawo linadzaza ndi achule
amene analowa m’zipinda zogona za olamulira awo.
31 Iye anayankhula, ndipo kunabwera ntchentche zochuluka
ndi nsabwe m’dziko lawo lonse.
32 Iyeyo anatembenuza mvula yawo kukhala matalala,
ndi zing’aning’ani m’dziko lawo lonse;
33 Anagwetsa mitengo yawo ya mpesa ndi mitengo yawo ya mkuyu,
nawononganso mitengo ina ya m’dziko lawolo.
34 Iye anayankhula, ndipo dzombe linabwera,
ziwala zosawerengeka;
35 zinadya chilichonse chobiriwira cha m’dziko lawo,
zinadya zonse zotuluka m’nthaka yawo.
36 Kenaka anakantha ana onse oyamba kubadwa a m’dziko lawo,
zipatso zoyamba za umunthu wawo wonse.

37 Yehova anatulutsa Israeli, atatenga siliva ndi golide wambiri,
ndipo pakati pa mafuko awo palibe mmodzi amene anafowoka.
38 Dziko la Igupto linakondwa pamene iwo anachoka,
pakuti kuopsa kwa Israeli kunawagwera iwo.
39 Iye anatambasula mitambo ngati chofunda chawo,
ndi moto owawunikira usiku.
40 Iwo anapempha, ndipo Iye anawabweretsera zinziri
ndipo anawakhutitsa ndi chakudya chochokera kumwamba.
41 Iye anatsekula thanthwe, ndipo madzi anatuluka;
ngati mtsinje anayenda m’chipululu.

42 Pakuti anakumbukira lonjezo lake loyera limene
linaperekedwa kwa Abrahamu mtumiki wake.
43 Iye anatulutsa anthu ake akukondwera,
osankhika ake akufuwula mwachimwemwe;
44 Iye anawapatsa mayiko a anthu a mitundu ina
ndipo anakhala olowam’malo a zimene ena anazivutikira,
45 kuti iwo asunge malangizo ake
ndi kutsatira malamulo ake.

Tamandani Yehova.

# Salimo 106

1 Tamandani Yehova.

Yamikani Yehova chifukwa ndi wabwino;
pakuti chikondi chake ndi chosatha.
2 Ndani angathe kufotokoza za ntchito zamphamvu za Yehova
kapena kumutamanda mokwanira?
3 Odala ndi amene amasunga chilungamo,
amene amachita zolungama nthawi zonse.
4 Mundikumbukire Yehova, pamene mukuonetsa kukoma mtima kwanu kwa anthu anu,
bwerani mudzandithandize pamene mukuwapulumutsa iwo,
5 kuti ndidzasangalale ndi chuma cha anthu anu osankhika,
kuti ndidzakhale nacho chimwemwe cha anthu anu

ndi kukhala pamodzi ndi cholowa chanu pa kukutamandani.

6 Ife tachimwa monga momwe anachitira makolo athu;
tachita zolakwa ndipo tachita moyipa.
7 Pamene makolo athu anali mu Igupto,
sanalingalire za zozizwitsa zanu;
iwo sanakumbukire kukoma mtima kwanu kochuluka,
ndipo anawukira Inu pa Nyanja Yofiira.
8 Komabe Iye anawapulumutsa chifukwa cha dzina lake,
kuti aonetse mphamvu zake zazikulu.
9 Anadzudzula Nyanja Yofiira, ndipo inawuma;
anawatsogolera m'nyanja yakuya ngati akuyenda m'chipululu.
10 Anawapulumutsa m'dzanja la amaliwongo;
anawawombola m'dzanja la mdani.
11 Madzi anamiza adani awo,
palibe mmodzi wa iwo anapulumuka.
12 Kenaka iwo anakhulupirira malonjezo ake
ndi kuyimba nyimbo zamatamando.

13 Koma posachedwa anayiwala zimene Iye anachita,
ndipo sanayembekezere uphungu wake.
14 M'chipululu, anadzipereka ku zilakolako zawo;
m'dziko lopanda kanthu anayesa Mulungu.
15 Choncho Iye anawapatsa chimene anapempha,
koma anatumiza nthenda yowondetsa.

16 M'misasa, anachitira nsanje Mose ndi Aaroni,
amene Yehova anadzipatulira.
17 Nthaka inatsekuka ndipo inameza Datani;
inakwirira gulu la Abiramu.
18 Moto unayaka pakati pa otsatira awo;
lawi lamoto linapsereza anthu oyipa.

19 Iwo anapanga mwana wang'ombe pa Horebu
ndi kulambira fano loyengedwa kuchokera ku chitsulo.
20 Anasinthanitsa ulemerero wawo
ndi fano la ng'ombe yayimuna imene imadya udzu.
21 Anayiwala Mulungu amene anawapulumutsa,
amene anachita zinthu zazikulu mu Igupto,
22 zozizwitsa m'dziko la Hamu
ndi machitidwe ake woopsa pa Nyanja Yofiira.
23 Choncho Iye anawawuza kuti adzawawononga,
pakanapanda Mose, mtumiki wake wosankhidwa,
kuyima pamaso pake,
ndi kuletsa mkwiyo wake kuti usawawononge.

24 Motero iwo ananyoza dziko lokoma;
sanakhulupirire malonjezo ake.
25 Anang'ung'udza m'matenti mwawo
ndipo sanamvere Yehova.
26 Kotero Iye analumbira atakweza dzanja lake,

kuti adzachititsa kuti iwowo afere m'chipululu,
27 kuchititsa kuti zidzukulu zawo zifere pakati pa anthu a mitundu ina
ndi kuwabalalitsa m'dziko lonse.

28 Iwo anayamba kupembedza Baala-Peori
ndi kudya nsembe zoperekedwa kwa milungu yopanda moyo;
29 anaputa mkwiyo wa Yehova pa machitidwe awo oyipa,
ndipo mliri unabuka pakati pawo.
30 Koma Finehasi anayimirira ndi kulowererapo,
ndipo mliri unaleka.
31 Chimenechi ndicho chinayesedwa chilungamo chake,
kwa mibado yosatha imene ikubwera.

32 Pa madzi a ku Meriba iwo anakwiyitsa Yehova
ndipo mavuto anabwera kwa Mose chifukwa cha anthuwo,
33 pakuti iwowo anawukira mzimu wa Mulungu,
ndipo pa milomo ya Mose panatuluka mawu osayenera.

34 Aisraeliwo sanawononge mitundu ya anthu
monga momwe Yehova anawalamulira.
35 Koma anasakanizana ndi anthu a mitundu inayo
ndi kuphunzira miyambo yawo.
36 Ndipo anapembedza mafano awo,
amene anakhala msampha kwa iwowo.
37 Anapereka nsembe ana awo aamuna
ndi ana awo aakazi kwa ziwanda.
38 Anakhetsa magazi a anthu osalakwa,
magazi a ana awo aamuna ndi a ana awo aakazi,
amene anawapereka nsembe kwa mafano a ku Kanaani,
ndipo dziko linayipitsidwa ndi magazi awo.
39 Iwo anadzidetsa okha ndi zimene anachita;
ndi machitidwe awo amakhala ngati munthu wachigololo.

40 Tsono Yehova anakwiya ndi anthu ake
ndipo ananyansidwa ndi cholowa chake.
41 Iye anawapereka kwa anthu a mitundu ina,
ndipo adani awo anawalamulira.
42 Adani awo anawazunza
ndi kuwakhazika pansi pa mphamvu yawo.
43 Iye ankawapulumutsa nthawi zambiri,
koma iwo ankatsimikiza za kuwukira
ndipo anawonongeka m'machimo awo.

44 Koma Iye anaona kuzunzika kwawo
pamene anamva kulira kwawo;
45 Chifukwa cha iwo Iye anakumbukira pangano lake
ndipo anawalezera mtima chifukwa cha kukula kwa chikondi chake.
46 Iye anachititsa kuti amene anawagwira iwo ukapolo
awamvere chisoni.

47 Tipulumutseni Inu Yehova Mulungu wathu,
ndipo mutisonkhanitse kuchoka kwa anthu a mitundu ina

kuti tithe kuyamika dzina lanu loyera
ndi kunyadira m'matamando anu.

48 Atamandike Yehova, Mulungu wa Israeli,
Kuyambira muyaya mpaka muyaya.
Anthu onse anene kuti, "Ameni!"

Tamandani Yehova.

## BUKU LACHISANU

## 107

*Masalimo 107–150*

1 Yamikani Yehova chifukwa ndi wabwino;
pakuti chikondi chake ndi chosatha.
2 Owomboledwa a Yehova anene zimenezi
amene Iyeyo anawawombola m'dzanja la mdani,
3 iwo amene anawasonkhanitsa kuchokera ku mayiko,
kuchokera kumadzulo ndi kummawa, kuchokera kumpoto ndi kummwera.

4 Ena anayendayenda m'chipululu mopanda kanthu,
osapeza njira yopitira ku mzinda kumene akanakakhazikikako.
5 Iwo anamva njala ndi ludzu,
ndipo miyoyo yawo inafowokeratu.
6 Pamenepo analirira Yehova m'mavuto awo
ndipo Iye anawapulumutsa ku masautso awo.
7 Iye anawatsogolera m'njira yowongoka
kupita ku mzinda umene anakakhazikikako.
8 Ayamike Yehova chifukwa cha chikondi chake chosatha
ndi chifukwa cha machitidwe ake odabwitsa kwa anthu onse,
9 pakuti Iye wapha ludzu la munthu womva ludzu
ndipo wakhutitsa wanjala ndi zinthu zabwino.

10 Ena anakhala mu mdima ndi m'chisoni chachikulu,
am'ndende ovutika m'maunyolo achitsulo,
11 pakuti iwowo anawukira mawu a Mulungu
ndi kunyoza uphungu wa Wammwambamwamba.
12 Kotero Iye anawapereka kuti agwire ntchito yakalavulagaga;
anagwa pansi ndipo panalibe woti awathandize.
13 Pamenepo analirira Yehova m'masautso awo
ndipo Iye anawapulumutsa ku masautso awo.
14 Yehova anawatulutsa mu mdima ndi m'chisoni chachikulu
ndipo anadula maunyolo awo.
15 Ayamike Yehova chifukwa cha chikondi chake chosatha
ndi machitidwe ake odabwitsa kwa anthu onse,
16 pakuti Iye amathyola zipata zamkuwa
ndi kudula pakati mipiringidzo yachitsulo.

17 Ena anakhala zitsiru chifukwa cha njira zawo zowukira,
ndipo anamva zowawa chifukwa cha mphulupulu zawo.
18 Iwo ananyansidwa ndi chakudya chilichonse
ndipo anafika pafupi ndi zipata za imfa.

19 Pamenepo analirira Yehova m'masautso awo
ndipo Iye anawapulumutsa ku masautso awowo.
20 Iye anatumiza mawu ake ndi kuwachiritsa;
anawalanditsa ku manda.
21 Ayamike Yehova chifukwa cha chikondi chake chosatha
ndi machitidwe ake odabwitsa kwa anthu.
22 Apereke nsembe yachiyamiko
ndi kufotokoza za ntchito zake ndi nyimbo zachimwemwe.

23 Ena anayenda pa nyanja m'sitima zapamadzi;
Iwo anali anthu amalonda pa nyanja yayikulu.
24 Anaona ntchito za Yehova,
machitidwe ake odabwitsa m'nyanja yakuya.
25 Pakuti Iye anayankhula ndi kuwutsa mphepo yamkuntho
imene inabweretsa mafunde ataliatali.
26 Sitima za pamadzizo zinatukulidwa mmwamba ndi kutsikira pansi pakuya;
pamene amawonongeka, kulimba mtima kwawo kunasungunuka.
27 Anachita chizungulire ndi kudzandira ngati anthu oledzera;
anali pa mapeto a moyo wawo.
28 Pamenepo analirira Yehova m'masautso awo
ndipo Iyeyo anawapulumutsa ku masautso awo.
29 Yehova analetsa namondwe,
mafunde a m'nyanja anatontholetsedwa.
30 Anali osangalala pamene kunakhala bata,
ndipo Iye anawatsogolera ku dooko limene amalifuna.
31 Ayamike Yehova chifukwa cha chikondi chake chosatha
ndi machitidwe ake odabwitsa kwa anthu.
32 Akuze Iye mu msonkhano wa anthu
ndi kumutamanda pabwalo la akuluakulu.

33 Iye anasandutsa mitsinje kukhala chipululu,
akasupe otuluka madzi kukhala nthaka yowuma,
34 ndiponso nthaka yachonde kukhala nthaka yamchere,
chifukwa cha kuyipa kwa amene amakhala kumeneko.
35 Anasandutsa chipululu kukhala mayiwe a madzi
ndi nthaka yowuma kukhala akasupe a madzi oyenda;
36 kumeneko Iye anabweretsa anthu anjala kuti azikhalako,
ndipo iwo anamanga mzinda woti akhazikikeko.
37 Anafesa mbewu m'minda ndi kudzala mipesa
ndipo anakolola zipatso zochuluka;
38 Yehova anawadalitsa, ndipo chiwerengero chawo chinachuluka kwambiri,
ndipo Iye sanalole kuti ziweto zawo zithe.

39 Kenaka chiwerengero chawo chinachepa ndipo iwo anatsitsidwa
chifukwa cha mazunzo, mavuto ndi chisoni;
40 Iye amene amakhuthulira m'nyozo pa olemekezeka
anawachititsa kuyendayenda m'malo owumawo wopanda njira.
41 Koma Iyeyo anakweza anthu osowa kuchoka ku masautso awo
ngati magulu a nkhosa.

42 Anthu olungama mtima amaona ndi kusangalala,
koma anthu onse oyipa amatseka pakamwa pawo.

43 Aliyense wanzeru asamalitse zinthu zimenezi
ndi kuganizira za chikondi chachikulu cha Yehova.

# Salimo 108

Nyimbo. Salimo la Davide.
1 Mtima wanga ndi wokhazikika, Inu Mulungu;
ndidzayimba nyimbo, inde ndidzayimba nyimbo zotamanda ndi moyo wanga wonse.
2 Dzukani, zeze ndi pangwe!
Ine ndidzadzutsa m'bandakucha.
3 Ndidzakutamandani Yehova, pakati pa anthu a mitundu ina;
ndidzayimba za Inu pakati pa anthu a mitundu ina.
4 Pakuti chikondi chanu n'chachikulu, kutalika kwake kuposa kumwamba;
kukhulupirika kwanu kumafika mlengalenga.
5 Kwezekani Inu Mulungu, kuposa mayiko akumwamba,
ndipo ulemerero wanu uphimbe dziko lonse lapansi.

6 Tipulumutseni ndi kutithandiza ndi dzanja lanu lamanja
kuti iwo amene mumawakonda apulumutsidwe.
7 Mulungu wayankhula kuchokera ku malo ake opatulika:
"Mwachipambano Ine ndidzagawa Sekemu
ndipo ndidzayesa chigwa cha Sukoti.
8 Giliyadi ndi wanga, Manase ndi wanganso;
Efereimu ndi chipewa changa chodzitetezera,
Yuda ndi ndodo yanga yaufumu.
9 Mowabu ndi mbale yanga yosambiramo
ndidzaponya nsapato zanga pa Edomu;
ndidzafuwula mopambana pa Filisitiya."

10 Ndani adzandifikitsa ku mzinda wotetezedwa?
Ndani adzanditsogolera ku Edomu?
11 Kodi sindinu Mulungu, Inu amene mwatikana
ndipo simuperekezanso magulu athu ankhondo?
12 Tithandizeni ife kulimbana ndi mdani,
pakuti thandizo la munthu ndi lopanda pake.
13 Chifukwa cha Mulungu wathu, ife tidzapeza chipambano,
ndipo adzapondereza pansi adani athu.

# Salimo 109

Kwa mtsogoleri wamayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Mulungu amene ndimakutamandani,
musakhale chete,
2 pakuti anthu oyipa ndi achinyengo
atsekula pakamwa pawo kutsutsana nane;
iwo ayankhula motsutsana nane ndi malilime abodza.
3 Andizungulira ndi mawu audani,
amandinena popanda chifukwa.
4 M'malo mwa chikondi changa amandineneza,

koma ine ndine munthu wapemphero.
5 Iwo amandibwezera zoyipa m'malo mwa zabwino,
ndi udani m'malo mwa chikondi changa.

6 Sankhani munthu woyipa kuti amutsutse iye;
lolani wotsutsa ayime ku dzanja lake lamanja.
7 Pamene aweruzidwa, apezeke kuti ndi wolakwa,
ndipo mapemphero ake amutsutse.
8 Masiku ake akhale owerengeka;
munthu wina atenge malo ake a utsogoleri.
9 Ana ake akhale amasiye
ndipo mkazi wake akhale wopanda mwamuna.
10 Ana ake akhale oyendayenda ndi opemphapempha;
apirikitsidwe kuchoka pa mabwinja a nyumba zawo.
11 Wokongoza alande zonse zimene ali nazo;
alendo afunkhe ntchito za manja ake.
12 Pasapezeke ndi mmodzi yemwe womukomera mtima
kapena kumvera chisoni ana ake amasiye.
13 Zidzukulu zake zithe n'kufa,
mayina awo afafanizidwe mu m'bado wotsatirawo.
14 Mphulupulu za makolo ake zikumbukiridwe pamaso pa Yehova;
tchimo la amayi ake lisadzafafanizidwe.
15 Machimo awo akhale pamaso pa Yehova nthawi zonse,
kuti Iye achotse chikumbutso chawo pa dziko lapansi.

16 Pakuti iye sanaganizirepo zochita chifundo,
koma anazunza mpaka kuwapha anthu osauka
ndi osweka mtima.
17 Anakonda kutemberera,
matembererowo abwerere kwa iye;
sanakondwe n'kudalitsa anthu ena,
choncho madalitso akhale kutali naye.
18 Anavala kutemberera ngati chovala;
kutemberera kunalowa m'thupi lake ngati madzi,
kulowa m'mafupa ake ngati mafuta.
19 Matemberero akhale ngati chofunda chodzikutira nacho,
ngati lamba wovala tsiku ndi tsiku.
20 Awa akhale malipiro ochokera kwa Yehova pa onditsutsa anga,
kwa iwo amene amayankhula zoyipa za ine.

21 Koma Inu Ambuye Wamphamvuzonse,
muchite nane molingana ndi dzina lanu,
chifukwa cha ubwino wa chikondi chanu, pulumutseni.
22 Pakuti ndine wosauka ndi wosowa,
ndipo mtima wanga ukuwawa m'kati mwanga.
23 Ndikuzimirira ngati mthunzi wa kumadzulo,
ndapirikitsidwa ngati dzombe.
24 Mawondo anga afowoka chifukwa cha kusala zakudya,
thupi langa lawonda ndi mutu wanga womwe.
25 Ndine chinthu chotonzedwa kwa otsutsana nane;
akandiona, amapukusa mitu yawo.

26 Thandizeni Inu Yehova Mulungu wanga;
pulumutseni molingana ndi chikondi chanu.
27 Adaniwo adziwe kuti limeneli ndi dzanja lanu,
kuti Inu Yehova mwachita zimenezi.
28 Angathe kutemberera, koma Inu mudzadalitsa;
pamene iwo andiputa adzachititsidwa manyazi,
koma mtumiki wanu adzasangalala.
29 Onditsutsa adzavekedwa mnyozo,
ndipo adzadzifunditsa manyazi ngati chovala.

30 Ndi pakamwa panga ndidzathokoza Yehova kwambiri;
ndidzamutamanda m'gulu lalikulu la anthu.
31 Popeza Iye amayima ku dzanja lamanja la munthu wosowayo,
kupulumutsa moyo wake kwa iwo amene agamula molakwa.

# Salimo 110

Salimo la Davide.
1 Yehova akuwuza Mbuye wanga kuti,
"Khala ku dzanja langa lamanja
mpaka nditasandutsa adani ako
kukhala chopondapo mapazi ako."

2 Yehova adzakuza ndodo yamphamvu ya ufumu wako kuchokera m'Ziyoni;
udzalamulira pakati pa adani ako.
3 Ankhondo ako adzakhala odzipereka
pa tsiku lako la nkhondo.
Atavala chiyero chaulemerero,
kuchokera m'mimba ya m'bandakucha,
udzalandira mame a unyamata wako.

4 Yehova walumbira
ndipo sadzasintha maganizo ake:
"Ndiwe wansembe mpaka muyaya
monga mwa unsembe wa Melikizedeki."

5 Ambuye ali kudzanja lako lamanja;
Iye adzaponda mafumu pa tsiku la ukali wake.
6 Adzaweruza anthu a mitundu ina,
adzadzaza dziko lapansi ndi mitembo ndipo adzaphwanya olamulira a pa dziko lonse lapansi.
7 Iye adzamwa mu mtsinje wa m'mbali mwa njira;
choncho adzaweramutsa mutu wake.

# Salimo 111

1 Tamandani Yehova.

Ndidzathokoza Yehova ndi mtima wanga wonse
m'bwalo la anthu olungama mtima ndi pa msonkhano.

2 Ntchito za Yehova n'zazikulu;
onse amene amakondwera nazo amazilingalira.

3 Zochita zake ndi za ulemerero ndi zaufumu,
ndipo chilungamo chake ndi chosatha.
4 Iye wachititsa kuti zodabwitsa zake zikumbukirike;
Yehova ndi wokoma mtima ndi wachifundo.
5 Amapereka chakudya kwa amene amamuopa Iye;
amakumbukira pangano lake kwamuyaya.
6 Waonetsa anthu ake mphamvu ya ntchito zake,
kuwapatsa mayiko a anthu a mitundu ina.
7 Ntchito za manja ake ndi zokhulupirika ndi zolungama;
malangizo ake onse ndi odalirika.
8 Malamulo ndi okhazikika ku nthawi za nthawi,
ochitidwa mokhulupirika ndi molungama.
9 Iyeyo amawombola anthu ake;
anakhazikitsa pangano lake kwamuyaya
dzina lake ndi loyera ndi loopsa.

10 Kuopa Yehova ndicho chiyambi cha nzeru;
onse amene amatsatira malangizo ake amamvetsa bwino zinthu.
Iye ndi wotamandika mpaka muyaya.

# Salimo 112

1 Tamandani Yehova.

Wodala munthu amene amaopa Yehova,
amene amakondwera kwambiri ndi malamulo ake.

2 Ana ake adzakhala amphamvu m'dziko;
m'bado wa olungama mtima udzadalitsidwa.
3 Kulemera ndi chuma zili m'nyumba yake,
ndipo chilungamo chake ndi chosatha.
4 Ngakhale mu mdima kuwala kumatulukira olungama mtima;
wokoma mtima, wachifundo ndi wowongoka mtima.
5 Zinthu zabwino zidzabwera kwa iye amene amapereka mowolowamanja
ndi wokongoletsa mwaufulu,
amene amachita ntchito yake mwachilungamo.

6 Ndithu sadzagwedezeka;
munthu wolungama sadzayiwalika mpaka muyaya.
7 Saopa akamva zoyipa zimene zachitika;
mtima wake ndi wokhazikika ndipo amadalira Yehova.
8 Mtima wake ndi wotetezedwa, sadzakhala ndi mantha;
potsiriza pake adzayang'ana adani ake mwachipambano.
9 Wopereka mphatso zake mowolowamanja kwa osauka,
chilungamo chake chimanka mpaka muyaya;
nyanga yake idzakwezedwa mwaulemu.

10 Munthu woyipa adzaona zimenezi ndipo adzapsa mtima;
adzakukuta mano ake ndipo adzasungunuka.
Zolakalaka za anthu oyipa sizidzachitika konse.

# Salimo 113

1 Tamandani Yehova.

Mutamandeni, inu atumiki a Yehova,
tamandani dzina la Yehova.
2 Yehova atamandidwe,
kuyambira tsopano mpaka muyaya.
3 Kuyambira ku matulukiro a dzuwa mpaka ku malowero ake,
dzina la Yehova liyenera kutamandidwa.

4 Yehova wakwezeka pa anthu a mitundu yonse,
ulemerero wake ndi woposa mayiko akumwamba.
5 Ndani wofanana ndi Yehova Mulungu wathu,
Iye amene amakhala mwaufumu mmwamba?
6 amene amawerama pansi kuyang'ana
miyamba ndi dziko lapansi?

7 Iye amakweza munthu wosauka kuchoka pa fumbi
ndi kutukula munthu wosowa kuchoka pa dzala;
8 amawakhazika pamodzi ndi mafumu,
pamodzi ndi mafumu a anthu ake.
9 Amakhazikitsa mayi wosabereka m'nyumba yake
monga mayi wa ana wosangalala.

Tamandani Yehova.

# Salimo 114

1 Pamene Israeli anatuluka mu Igupto,
nyumba ya Yakobo kuchoka ku mtundu wa anthu a chiyankhulo chachilendo,
2 Yuda anasanduka malo opatulika a Mulungu,
Israeli anasanduka ufumu wake.

3 Nyanja inaona ndi kuthawa,
mtsinje wa Yorodani unabwerera m'mbuyo;
4 mapiri analumphalumpha ngati nkhosa zazimuna,
timapiri ngati ana ankhosa.

5 N'chifukwa chiyani iwe unathawa?
iwe mtsinje wa Yorodani unabwereranji m'mbuyo?
6 inu mapiri, munalumphalumphiranji ngati nkhosa zazimuna,
inu timapiri, ngati ana ankhosa?

7 Njenjemera pamaso pa Ambuye iwe dziko lapansi,
pamaso pa Mulungu wa Yakobo,
8 amene anasandutsa thanthwe kukhala chitsime,
thanthwe lolimba kukhala akasupe a madzi.

# Salimo 115

1 Kwa ife ayi Yehova, kwa ife ayi
koma ulemerero ukhale pa dzina lanu,
chifukwa cha chikondi chanu chosasinthika ndiponso chifukwa cha kukhulupirika kwanu.

2 Chifukwa chiyani anthu a mitundu ina akunena kuti,

“Mulungu wawo ali kuti?”
3 Mulungu wathu ali kumwamba;
Iye amachita chilichonse chimene chimamukondweretsa.
4 Koma mafano awo ndi siliva ndi golide,
opangidwa ndi manja a anthu.
5 Pakamwa ali napo koma sayankhula,
maso ali nawo koma sapenya;
6 makutu ali nawo koma samva,
mphuno ali nazo koma sanunkhiza;
7 manja ali nawo koma akakhudza samva kanthu;
mapazi ali nawo koma sayenda;
kapena pakhosi pawo kutulutsa mawu.
8 Anthu amene amapanga mafanowo adzafanana nawo,
chimodzimodzinso onse amene amadalira mafanowo.

9 Inu Aisraeli, dalirani Yehova;
Iye ndiye thandizo lanu ndi chishango chanu.
10 Iwe nyumba ya Aaroni, dalira Yehova;
Iye ndiye thandizo lako ndi chishango chako.
11 Inu amene mumaopa Iye, dalirani Yehova;
Iye ndiye thandizo lanu ndi chishango chanu.

12 Yehova watikumbukira ndipo adzatidalitsa:
adzadalitsa nyumba ya Israeli,
adzadalitsa nyumba ya Aaroni,
13 adzadalitsa iwo amene amaopa Yehova;
aang’ono ndi aakulu omwe.

14 Yehova akuwonjezereni madalitso;
inuyo pamodzi ndi ana anu.
15 Mudalitsidwe ndi Yehova,
Wolenga kumwamba ndi dziko lapansi.

16 Kumwamba ndi kwa Yehova,
koma dziko lapansi Iye walipereka kwa anthu.
17 Si anthu akufa amene amatamanda Yehova,
amene amatsikira kuli chete;
18 ndi ife amene timatamanda Yehova,
kuyambira tsopano mpaka muyaya.

Tamandani Yehova.

# Salimo 116

1 Ndimakonda Yehova pakuti Iyeyo amamva mawu anga;
Iye amamva kulira kwanga kopempha chifundo.
2 Pakuti ananditchera khutu,
ndidzayitana Iye masiku onse a moyo wanga.

3 Zingwe za imfa zinandizinga,
zoopsa za ku dziko la anthu akufa zinandigwera;
ndinapeza mavuto ndi chisoni.
4 Pamenepo ndinayitana dzina la Yehova:

“Inu Yehova, pulumutseni!”

5 Yehova ndi wokoma mtima ndi wolungama
Mulungu wathu ndi wodzaza ndi chifundo.
6 Yehova amateteza munthu wodzichepetsa mtima;
pamene ndinali ndi chosowa chachikulu, Iye anandipulumutsa.

7 Pumula iwe moyo wanga,
pakuti Yehova wakuchitira zokoma.

8 Pakuti Inu Yehova mwapulumutsa moyo wanga ku imfa,
maso anga ku misozi,
mapazi anga kuti angapunthwe,
9 kuti ine ndiyende pamaso pa Yehova
m’dziko la anthu amoyo.
10 Ine ndinakhulupirira; choncho ndinati,
“Ndasautsidwa kwambiri.”
11 Ndipo ndili m’nkhawa yanga ndinati,
“Anthu onse ndi abodza.”

12 Ndingamubwezere chiyani Yehova,
chifukwa cha zokoma zake zonse zimene wandichitira?
13 Ndidzakweza chikho cha chipulumutso
ndipo ndidzayitana dzina la Yehova.
14 Ndidzakwaniritsa malonjezo anga kwa Yehova
pamaso pa anthu ake onse.

15 Imfa ya anthu oyera mtima
ndi yamtengowapatali pamaso pa Yehova.
16 Inu Yehova, zoonadi ndine mtumiki wanu:
ndine mtumiki wanu, mwana wa mdzakazi wanu;
Inu mwamasula maunyolo anga.

17 Ndidzapereka nsembe yachiyamiko kwa Inu
ndipo ndidzayitanira pa dzina la Yehova.
18 Ndidzakwaniritsa malonjezo anga kwa Yehova
pamaso pa anthu ake onse,
19 m’mabwalo a nyumba ya Yehova,
m’kati mwako iwe Yerusalemu.

Tamandani Yehova.

# Salimo 117

1 Tamandani Yehova, inu anthu a mitundu yonse;
mulemekezeni Iye, inu mitundu ya anthu.
2 Pakuti chikondi chake pa ife ndi chachikulu,
ndipo kukhulupirika kwa Yehova n’kosatha.

Tamandani Yehova.

# Salimo 118

1 Yamikani Yehova chifukwa ndi wabwino;

pakuti chikondi chake chosasinthika ndi chosatha.

2 Israeli anene kuti:
“Chikondi chake ndi chosatha.”
3 Banja la Aaroni linene kuti,
“Chikondi chake ndi chosatha.”
4 Iwo amene amaopa Yehova anene kuti:
“Chikondi chake ndi chosatha.”

5 Ndili m’masautso anga ndinalirira Yehova,
ndipo Iye anayankha pondichotsa m’masautsowo.
6 Yehova ali nane; sindidzachita mantha.
Munthu angandichite chiyani?
7 Yehova ali nane; Iye ndiye thandizo langa.
Ndidzayang’ana adani anga mwachipambano.

8 N’kwabwino kuthawira kwa Yehova
kusiyana ndi kudalira munthu.
9 N’kwabwino kuthawira kwa Yehova
kusiyana ndi kudalira mafumu.

10 Anthu a mitundu yonse anandizinga,
koma m’dzina la Yehova ndinawawononga.
11 Anandizinga mbali zonse,
koma m’dzina la Yehova ndinawawononga.
12 Anandizinga ngati njuchi,
koma anatha msanga ngati moto wapaminga;
m’dzina la Yehova ndinawawononga.

13 Anandikankha uku ndi uko ndipo ndinali pafupi kugwa,
koma Yehova ananditha ndiza.
14 Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga;
Iye wakhala chipulumutso changa.

15 Mfuwu wachimwemwe ndi chipambano
ukumveka m’matenti a anthu olungama mtima kuti:
“Dzanja lamanja la Yehova lachita zamphamvu!
16 Dzanja lamanja la Yehova latukulidwa mmwamba
Dzanja lamanja la Yehova lachita zamphamvu!”

17 Sindidzafa koma ndidzakhala ndi moyo
ndipo ndidzalalika za ntchito ya Yehova.
18 Yehova wandilanga koopsa,
koma sanandipereke ku imfa.

19 Tsekulireni zipata zachilungamo,
kuti ndifike kudzayamika Yehova.
20 Ichi ndicho chipata cha Yehova
chimene olungama mtima okha adzalowerapo.
21 Ndidzakuyamikani chifukwa Inu munandiyankha;
mwakhala chipulumutso changa.

22 Mwala umene amisiri omanga nyumba anawukana
wasanduka wapangodya;
23 Yehova ndiye wachita zimenezi
ndipo n'zodabwitsa pamaso pathu.
24 Lero ndiye tsiku limene Yehova walipanga;
tiyeni tikondwere ndi kusangalala nalo.

25 Inu Yehova, tipulumutseni;
Yehova, tipambanitseni.
26 Wodala amene akubwera m'dzina la Yehova.
Tikukudalitsani kuchokera ku nyumba ya Yehova.
27 Yehova ndi Mulungu,
ndipo kuwala kwake kwatiwunikira Ife.
Lowani nawo pa m'dipiti wa ku chikondwerero mutanyamula nthambi m'dzanja lanu,
mpaka ku nyanga za guwa.

28 Inu ndinu Mulungu wanga, ndipo ndidzakuyamikani;
Inu ndinu Mulungu wanga, ndipo ndidzakukwezani.

29 Yamikani Yehova chifukwa ndi wabwino;
pakuti chikondi chake chosasinthika ndi chosatha.

# Salimo 119

*Alefu*

1 Odala ndi amene moyo wawo ulibe cholakwa,
amene amayenda monga mwa malamulo a Yehova.
2 Odala ndi amene amasunga malamulo ake,
amene amafunafuna Iyeyo ndi mtima wawo wonse.
3 Sachita cholakwa chilichonse;
amayenda m'njira zake.
4 Inu mwapereka malangizo
ndipo ayenera kutsatidwa kwathunthu.
5 Aa! Ndikanakonda njira zanga zikanakhala zokhazikika
pa kumvera zophunzitsa zanu!
6 Pamenepo ine sindikanachititsidwa manyazi,
poganizira malamulo anu onse.
7 Ndidzakutamandani ndi mtima wolungama,
pamene ndikuphunzira malamulo anu olungama.
8 Ndidzamvera zophunzitsa zanu;
musanditaye kwathunthu.

*Beti*

9 Kodi mnyamata angathe bwanji kuyeretsa mayendedwe ake?
Akawasamala potsata mawu anu.
10 Ndimakufunafunani ndi mtima wanga wonse;
musalole kuti ndisochere kuchoka pa malamulo anu.
11 Ndasunga mawu anu mu mtima mwanga
kuti ndisakuchimwireni.
12 Mutamandike Inu Yehova;
phunzitseni malamulo anu.
13 Ndi milomo yanga ndimafotokoza malamulo anu onse

amene amachokera pakamwa panu.
14 Ndimakondwera potsatira malamulo anu
monga momwe munthu amakondwera akakhala ndi chuma chambiri.
15 Ndimalingalira malangizo anu
ndipo ndimaganizira njira zanu.
16 Ndimakondwera ndi malamulo anu;
sindidzayiwala konse mawu anu.

*Gimeli*

17 Chitirani zokoma mtumiki wanu, ndipo ndidzakhala ndi moyo;
kuti tsono ndisunge mawu anu.
18 Tsekulani maso anga kuti ndithe kuona
zinthu zodabwitsa m'malamulo anu.
19 Ine ndine mlendo pa dziko lapansi;
musandibisire malamulo anu.
20 Moyo wanga wafowoka polakalaka
malamulo anu nthawi zonse.
21 Inu mumadzudzula onyada, otembereredwa,
amene achoka pa malamulo anu.
22 Mundichotsere chitonzo ndi mnyozo
pakuti ndimasunga malamulo anu.
23 Ngakhale mafumu akhale pamodzi kundinyoza,
mtumiki wanu adzalingalirabe zophunzitsa zanu.
24 Malamulo anu amandikondweretsa;
ndiwo amene amandilangiza.

*Daleti*

25 Moyo wanga wakangamira fumbi;
tsitsimutseni molingana ndi mawu anu.
26 Ndinafotokoza njira zanga ndipo Inu munandiyankha;
phunzitseni malamulo anu.
27 Mundidziwitse chiphunzitso cha malangizo anu;
pamenepo ndidzalingalira zodabwitsa zanu.
28 Moyo wanga wafowoka ndi chisoni;
limbikitseni monga mwa mawu anu.
29 Mundichotse m'njira zachinyengo;
mundikomere mtima pondiphunzitsa malamulo anu.
30 Ndasankha njira ya choonadi;
ndayika malamulo anu pa mtima panga.
31 Ndagwiritsitsa umboni wanu, Inu Yehova;
musalole kuti ndichititsidwe manyazi.
32 Ndimathamanga m'njira ya malamulo anu,
pakuti Inu mwamasula mtima wanga.

*He*

33 Yehova, phunzitseni kutsatira zophunzitsa zanu;
ndipo ndidzazisunga mpaka kumapeto.
34 Mundipatse mtima womvetsa zinthu ndipo ndidzasunga malamulo anu
ndi kuwamvera ndi mtima wanga wonse.
35 Munditsogolere m'njira ya malamulo anu,
pakuti m'menemo ndimapezamo chikondwerero changa.
36 Tembenuzani mtima wanga kuti uzikonda malamulo anu,
osati chuma.
37 Tembenuzani maso anga kuchoka ku zinthu zachabechabe;
sungani moyo wanga monga mwa mawu anu.

38 Kwaniritsani lonjezo lanu kwa mtumiki wanu,
kuti Inu muopedwe.
39 Mundichotsere chipongwe chimene ndikuchiopa,
pakuti malamulo anu ndi abwino.
40 Taonani, ndimalakalakatu malangizo anu!
Sungani moyo wanga m’chilungamo chanu.

*Wawi*

41 Chikondi chanu chosasinthika chibwere kwa ine, Inu Yehova,
chipulumutso chanu monga mwa lonjezo lanu;
42 ndipo ndidzayankha amene amandinyoza,
popeza ndimadalira mawu anu.
43 Musakwatule mawu a choonadi m’kamwa mwanga,
pakuti ndakhazikitsa chiyembekezo changa m’malamulo anu.
44 Ndidzasunga malamulo anu nthawi zonse,
ku nthawi za nthawi.
45 Ndidzayendayenda mwaufulu,
chifukwa ndinafunafuna malangizo anu.
46 Ndidzayankhula za umboni wanu pamaso pa mfumu
ndipo sindidzachititsidwa manyazi,
47 popeza ndimakondwera ndi malamulo anu
chifukwa ndimawakonda.
48 Ndikweza manja anga ku malamulo anu, ku malamulo amene ndimawakonda,
ndipo ndimalingalira malangizo anu.

*Zayini*

49 Kumbukirani mawu anu kwa mtumiki wanu,
popeza mwandipatsa chiyembekezo.
50 Chitonthozo changa pa masautso anga ndi ichi:
lonjezo lanu limasunga moyo wanga.
51 Odzikuza amandinyoza popanda chowaletsa,
koma sindichoka pa malamulo anu.
52 Ndimakumbukira malamulo anu Yehova akalekale,
ndipo mwa iwo ndimapeza chitonthozo.
53 Ndayipidwa kwambiri chifukwa cha oyipa
amene ataya malamulo anu.
54 Zophunzitsa zanu ndi mitu ya nyimbo yanga
kulikonse kumene ndigonako.
55 Usiku ndimakumbukira dzina lanu Yehova,
ndipo ndidzasunga malamulo anu.
56 Ichi ndicho ndakhala ndikuchita:
ndimasunga malangizo anu.

*Heti*

57 Yehova, Inu ndiye gawo langa;
ndalonjeza kumvera mawu anu.
58 Ndimafunafuna nkhope yanu ndi mtima wanga wonse;
mundikomere mtima monga mwa lonjezo lanu.
59 Ndinalingalira za njira zanga
ndipo ndatembenuza mayendedwe anga kutsatira umboni wanu.
60 Ndidzafulumira ndipo sindidzazengereza
kumvera malamulo anu.
61 Ngakhale oyipa andimange ndi zingwe,
sindidzayiwala lamulo lanu.

62 Ndimadzuka pakati pa usiku kuyamika Inu
chifukwa cha malamulo anu olungama.
63 Ine ndine bwenzi la onse amene amakukondani,
kwa onse amene amatsatira malangizo anu.
64 Dziko lapansi ladzaza ndi chikondi chanu chosasinthika,
phunzitseni malamulo anu.

*Teti*

65 Inu Yehova, chitirani chabwino mtumiki wanu
molingana ndi mawu anu.
66 Phunzitseni nzeru ndi chiweruzo chabwino,
pakuti ndimakhulupirira malamulo anu.
67 Ndisanayambe kuzunzika ndinasochera,
koma tsopano ndimamvera mawu anu.
68 Inu ndinu abwino ndipo zimene mumachita ndi zabwino;
phunzitseni malamulo anu.
69 Ngakhale odzikuza andipaka mabodza,
ine ndimasunga malangizo anu ndi mtima wanga wonse.
70 Mitima yawo ndi yowuma ndi yosakhudzidwa,
koma ine ndimakondwera ndi malamulo anu.
71 Ndi bwino kuti ndinasautsidwa
kuti ndithe kuphunzira malamulo anu.
72 Lamulo lochokera m'kamwa mwanu limandikomera kwambiri
kuposa ndalama zambirimbiri za siliva ndi golide.

*Yodi*

73 Manja anu anandilenga ndi kundiwumba;
patseni nzeru zomvetsa zinthu kuti ndiphunzire malamulo anu.
74 Iwo amene amakuopani akondwere akandiona,
chifukwa chiyembekezo changa chili m'mawu anu.
75 Ine ndikudziwa, Inu Yehova, kuti malamulo anu ndi olungama
ndipo mwandizunza chifukwa cha kukhulupirika kwanu.
76 Chikondi chanu chosasinthika chikhale chitonthozo changa,
molingana ndi lonjezo lanu kwa mtumiki wanu.
77 Chifundo chanu chindifikire kuti ndikhale ndi moyo,
popeza malamulo anu ndiye chikondwerero changa.
78 Odzikuza achititsidwe manyazi chifukwa cha kundilakwira popanda chifukwa;
koma ine ndidzalingalira malangizo anu.
79 Iwo amene amakuopani atembenukire kwa ine,
iwo amene amamvetsetsa umboni wanu.
80 Mtima wanga ukhale wopanda cholakwa pa chiphunzitso chanu
kuti ndisachititsidwe manyazi.

*Kafu*

81 Moyo wanga wafowoka ndi kufunafuna chipulumutso chanu,
koma chiyembekezo changa chili m'mawu anu.
82 Maso anga alefuka pofunafuna lonjezo lanu;
Ine ndikuti, "Kodi mudzanditonthoza liti?"
83 Ngakhale ndili ngati thumba lachikopa la vinyo pa utsi
sindiyiwala zophunzitsa zanu.
84 Kodi mtumiki wanu ayenera kudikira mpaka liti?
Kodi mudzawalanga liti amene amandizunza?
85 Anthu osalabadira za Mulungu,

odzikuza amandikumbira dzenje motsutsana ndi malamulo anu.
86 Malamulo anu onse ndi odalirika;
thandizeni, pakuti anthu akundizunza popanda chifukwa.
87 Iwo anatsala pang'ono kundichotsa pa dziko lapansi
koma sindinataye malangizo anu.
88 Sungani moyo wanga molingana ndi chikondi chanu chosasinthika,
ndipo ndidzamvera umboni wa pakamwa panu.

*Lamedi*

89 Mawu anu Yehova ndi amuyaya;
akhazikika kumwambako.
90 Kukhulupirika kwanu kumakhala mpaka ku mibado yonse;
Inu munakhazikitsa dziko lapansi ndipo lilipobe.
91 Malamulo anu alipobe mpaka lero lino,
pakuti zinthu zonse zimatumikira Inu.
92 Malamulo anu akanapanda kukhala chikondwerero changa,
ndikanawonongeka m'masautso anga.
93 Ine sindidzayiwala konse malangizo anu,
pakuti ndi malangizo anuwo munasunga moyo wanga.
94 Ndine wanu, ndipulumutseni;
pakuti ndasamala malangizo anu.
95 Anthu oyipa akudikira kuti andiwononge,
koma ndidzalingalira umboni wanu.
96 Ndadziwa kuti zinthu zonse zili ndi malire,
koma malamulo anu alibe malire konse.

*Memu*

97 Ndithu, ine ndimakonda malamulo anu!
Ndimalingaliramo tsiku lonse.
98 Malamulo anu amachititsa kuti ndikhale wanzeru kuposa adani anga,
popeza malamulowo ali ndi ine nthawi zonse.
99 Ndimamvetsa zinthu kwambiri kuposa aphunzitsi anga onse
popeza ndimalingalira umboni wanu.
100 Ndili ndi nzeru zochuluka zomvetsera zinthu kuposa anthu okalamba,
popeza ndimamvera malangizo anu.
101 Ndimaletsa miyendo yanga kuyenda m'njira iliyonse yoyipa
kuti ndithe kumvera mawu anu.
102 Sindinapatuke kuchoka pa malamulo anu,
pakuti Inu mwini munandiphunzitsa.
103 Mawu anu ndi otsekemera ndikawalawa,
otsekemera kuposa uchi m'kamwa mwanga!
104 Ndimapeza nzeru zodziwira zinthu kuchokera m'malangizo anu;
kotero ndimadana ndi njira iliyonse yoyipa.

*Nuni*

105 Mawu anu ndi nyale ya kumapazi kwanga
ndi kuwunika kwa pa njira yanga.
106 Ndalumbira ndipo ndatsimikiza,
kuti ndidzatsatira malamulo anu olungama.
107 Ndazunzika kwambiri;
Inu Yehova, sungani moyo wanga molingana ndi mawu anu.
108 Inu Yehova, landirani matamando aufulu ochokera pakamwa panga,
ndipo ndiphunzitseni malamulo anu.
109 Ngakhale moyo wanga umakhala m'zoopsa nthawi ndi nthawi,
sindidzayiwala malamulo anu.

110 Anthu oyipa anditchera msampha,
koma sindinasochere kuchoka pa malangizo anu.
111 Umboni wanu ndiye cholowa changa kwamuyaya;
Iwo ndiye chimwemwe cha mtima wanga.
112 Mtima wanga wakhazikika pa kusunga zophunzitsa zanu
mpaka kumapeto kwenikweni.

*Samekhi*

113 Ndimadana ndi anthu apawiripawiri,
koma ndimakonda malamulo anu.
114 Inu ndinu pothawirapo panga ndi chishango changa;
chiyembekezo changa chili m'mawu anu.
115 Chokani kwa ine, inu anthu ochita zoyipa,
kuti ndisunge malamulo a Mulungu wanga!
116 Mundichirikize molingana ndi lonjezo lanu, ndipo ndidzakhala ndi moyo;
musalole kuti chiyembekezo changa chipite pachabe.
117 Gwirizizeni, ndipo ndidzapulumutsidwa;
nthawi zonse ndidzasamalira zophunzitsa zanu.
118 Inu mumakana onse amene amasochera kuchoka pa zophunzitsa zanu,
pakuti chinyengo chawo ndi chopanda phindu.
119 Anthu onse oyipa a pa dziko lapansi mumawayesa ngati zinthu zakudzala;
n'chifukwa chake ndimakonda umboni wanu.
120 Thupi langa limanjenjemera chifukwa cha kuopa Inu;
ndimachita mantha ndi malamulo anu.

*Ayini*

121 Ndachita zolungama ndi zabwino;
musandisiye m'manja mwa ondizunza.
122 Onetsetsani kuti mtumiki wanu akukhala bwino,
musalole kuti anthu odzikuza andipondereze.
123 Maso anga alefuka, kufunafuna chipulumutso chanu,
kufunafuna lonjezo lanu lolungama.
124 Muchite naye mtumiki wanu molingana ndi chikondi chanu chosasinthika,
ndipo mundiphunzitse malamulo anu.
125 Ine ndine mtumiki wanu; patseni mzimu wondizindikiritsa,
kuti ndimvetsetse umboni wanu.
126 Yehova, ndi nthawi yoti muchitepo kanthu;
malamulo anu akuswedwa.
127 Chifukwa choti ndimakonda malamulo anu
kuposa golide, kuposa golide woyengeka bwino,
128 ndiponso chifukwa choti ndimaona kuti malangizo anu onse ndi wowongoka,
ndimadana ndi njira iliyonse yoyipa.

*Pe*

129 Maumboni anu ndi odabwitsa
n'chifukwa chake ndimawamvera.
130 Mawu anu akamaphunzitsidwa amapereka kuwunika;
ngakhale anthu wamba amamvetsetsa.
131 Ndimatsekula pakamwa panga ndi kupuma wefuwefu,
kufunafuna malamulo anu.
132 Tembenukirani kwa ine ndipo mundichitire chifundo,

monga mumachitira nthawi zonse kwa iwo amene amakonda dzina lanu.
133 Tsogolerani mayendedwe anga molingana ndi mawu anu;
musalole kuti tchimo lizindilamulira.
134 Ndiwomboleni m'dzanja la anthu ondizunza,
kuti ndithe kumvera malangizo anu.
135 Nkhope yanu iwalire mtumiki wanu
ndipo mundiphunzitse malamulo anu.
136 Mitsinje ya misozi ikuyenda kuchoka m'maso mwanga,
chifukwa anthu sakumvera malamulo anu.

*Tsade*

137 Yehova ndinu wolungama,
ndipo malamulo anu ndi abwino.
138 Maumboni amene munatipatsa ndi olungama;
ndi odalirika ndithu.
139 Ndikusautsidwa kwambiri m'kati mwanga
chifukwa adani anu amanyalanyaza mawu anu.
140 Mawu anu ndi woyera kwambiri
n'chifukwa chake mtumiki wanune ndimawakonda.
141 Ngakhale ndili wamng'ono ndi wonyozeka,
sindiyiwala malangizo anu.
142 Chilungamo chanu n'chamuyaya,
ndipo malamulo anu n'choona.
143 Mavuto ndi masautso zandigwera,
koma ndimakondwera ndi malamulo anu.
144 Umboni wanu ndi wabwino nthawi zonse;
patseni nzeru zomvetsa zinthu kuti ine ndikhale ndi moyo.

*Kofu*

145 Ndimayitana ndi mtima wanga wonse; ndiyankheni Inu Yehova,
ndipo ndidzamvera zophunzitsa zanu.
146 Ndikuyitana kwa Inu; pulumutseni
ndipo ndidzasunga umboni wanu.
147 Ndimadzuka tambala asanalire kuti ndipemphe thandizo;
chiyembekezo changa chili m'mawu anu.
148 Maso anga amakhala chipenyere nthawi yonse ya usiku,
kuti ndithe kulingalira malonjezo anu.
149 Imvani mawu anga molingana ndi chikondi chanu chosasinthika;
Yehova sungani moyo wanga, molingana ndi malamulo anu.
150 Iwo amene amakonza njira zoyipa andiyandikira,
koma ali kutali ndi malamulo anu.
151 Koma Inu Yehova muli pafupi,
malamulo anu onse ndi woona.
152 Ndinaphunzira kalekale kuchokera m'maumboni anu
kuti maumboni amene munakhazikitsawo ndi amuyaya.

*Reshi*

153 Yang'anani masautso anga ndipo mundipulumutse,
pakuti sindinayiwale malamulo anu.
154 Mundiyimirire pa mlandu wanga ndi kundiwombola;
sungani moyo wanga molingana ndi lonjezo lanu.
155 Chipulumutso chili kutali ndi anthu oyipa,
pakuti iwowo safunafuna zophunzitsa zanu.
156 Chifundo chanu Yehova n'chachikulu;

sungani moyo wanga molingana ndi malamulo anu.
157 Adani amene akundizunza ndi ambiri,
koma ine sindinatembenuke kuchoka pa umboni wanu.
158 Ndimawayang'ana monyansidwa anthu opanda chikhulupiriro,
popeza samvera mawu anu.
159 Onani momwe ndimakondera malangizo anu;
sungani moyo wanga, Inu Yehova, molingana ndi chikondi chanu chosanthika.
160 Mawu anu onse ndi owona;
malamulo anu onse olungama ndi amuyaya.

*Sini ndi Shini*

161 Olamulira amandizunza popanda chifukwa,
koma mtima wanga umanjenjemera ndi mawu anu.
162 Ine ndimakondwa ndi lonjezo lanu,
ngati munthu amene wapeza chuma chambiri.
163 Ndimadana ndi chinyengo, kwambiri ndimanyansidwa nacho,
koma ndimakonda malamulo anu.
164 Ndimakutamandani kasanu ndi kawiri pa tsiku
pakuti malamulo anu ndi olungama.
165 Amene amakonda malamulo anu ali ndi mtendere waukulu,
ndipo palibe chimene chingawapunthwitse
166 Ndikudikira chipulumutso chanu, Inu Yehova,
ndipo ndimatsatira malamulo anu.
167 Ndimamvera umboni wanu
pakuti ndimawukonda kwambiri.
168 Ndimamvera malangizo anu ndi umboni wanu,
pakuti njira zanga zonse ndi zodziwika pamaso panu.

*Tawu*

169 Kulira kwanga kufike pamaso panu Yehova;
patseni nzeru zomvetsa zinthu molingana ndi mawu anu.
170 Kupempha kwanga kufike pamaso panu;
pulumutseni molingana ndi lonjezo lanu.
171 Matamando asefukire pa milomo yanga,
pakuti Inu mumandiphunzitsa malamulo anu.
172 Lilime langa liyimbe mawu anu,
popeza malamulo anu onse ndi olungama.
173 Dzanja lanu likhale lokonzeka kundithandiza
pakuti ndasankha malangizo anu.
174 Ndikufunitsitsa chipulumutso chanu Yehova,
ndipo ndimakondwera ndi malamulo anu.
175 Loleni kuti ndikhale ndi moyo kuti ndikutamandeni,
ndipo malamulo anu andichirikize.
176 Ndasochera ngati nkhosa yotayika,
funafunani mtumiki wanu,
pakuti sindinayiwale malamulo anu.

# Salimo 120

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Ndimafuwulira kwa Yehova m'masautso anga,
ndipo Iye amandiyankha.
2 Pulumutseni Yehova ku milomo yabodza,
ndi kwa anthu achinyengo.

3 Kodi adzakuchitani chiyani,
ndipo adzawonjezerapo zotani, inu anthu achinyengo?
4 Adzakulangani ndi mivi yakuthwa ya munthu wankhondo,
ndi makala oyaka a mtengo wa tsanya.

5 Tsoka ine kuti ndimakhala ku Mesaki,
kuti ndimakhala pakati pa matenti a ku Kedara!
6 Kwa nthawi yayitali ndakhala pakati
pa iwo amene amadana ndi mtendere.
7 Ine ndine munthu wamtendere;
koma ndikamayankhula, iwo amafuna nkhondo.

# Salimo 121

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Ndikweza maso anga ku mapiri;
kodi thandizo langa limachokera kuti?
2 Thandizo langa limachokera kwa Yehova,
wolenga kumwamba ndi dziko lapansi.

3 Sadzalola kuti phazi lako literereke;
Iye amene amakusunga sadzawodzera.
4 Taonani, Iye amene amasunga Israeli
sadzawodzera kapena kugona.

5 Yehova ndiye amene amakusunga;
Yehova ndiye mthunzi wako ku dzanja lako lamanja.
6 Dzuwa silidzakupweteka nthawi ya masana,
kapena mwezi nthawi ya usiku.

7 Yehova adzakuteteza ku zoyipa zonse;
adzasunga moyo wako.
8 Yehova adzayang'anira kutuluka kwako ndi kulowa kwako;
kuyambira tsopano mpaka muyaya.

# Salimo 122

Salimo la Davide. Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Ndinakondwera atandiwuza kuti,
"Tiyeni ku nyumba ya Yehova."
2 Mapazi athu akuyima m'zipata
zako, Iwe Yerusalemu.

3 Yerusalemu anamangidwa ngati mzinda
umene uli wothithikana pamodzi.
4 Kumeneko ndiye kumene kumapita mafuko,
mafuko a Yehova,
umboni wa kwa Israeli,
kuti atamande dzina la Yehova.
5 Kumeneko anayikako mipando yaufumu yachiweruzo,
mipando yaufumu ya nyumba ya Davide.

6 Pemphererani mtendere wa Yerusalemu:

"Iwo amene amakukonda iwe zinthu ziwayendere bwino.
7 Mukhale mtendere m'kati mwa makoma ako,
ndipo m'nyumba zako zaufumu mukhale chitetezo."
8 Chifukwa cha abale anga ndi abwenzi anga
ndidzati, "Mtendere ukhale m'kati mwako."
9 Chifukwa cha Nyumba ya Yehova Mulungu wathu,
ndidzakufunira zabwino.

# Salimo 123

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Ndikweza maso anga kwa Inu,
kwa Inu amene mumakhala kumwamba.
2 Taonani, monga momwe maso a akapolo amayang'ana m'dzanja la mbuye wawo,
monga momwenso maso a mdzakazi amayang'ana m'dzanja la dona wake,
choncho maso athu ali kwa Yehova Mulungu wathu,
mpaka atichitire chifundo.

3 Mutichitire chifundo, Inu Yehova mutichitire chifundo,
pakuti tapirira chitonzo chachikulu.
4 Ife tapirira mnyozo wambiri kuchokera kwa anthu odzikuza,
chitonzo chachikulu kuchokera kwa anthu onyada.

# Salimo 124

Salimo la Davide. Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Akanapanda kukhala mbali yathu Yehova,
anene tsono Israeli,
2 akanapanda kukhala mbali yathu Yehova,
potiwukira anthuwo,
3 iwo atatipsera mtima,
akanatimeza amoyo;
4 chigumula chikanatimiza,
mtsinje ukanatikokolola,
5 madzi a mkokomo
akanatikokolola.

6 Atamandike Yehova,
amene sanalole kuti tikhale chakudya cha mano awo.
7 Moyo wathu wawonjoka ngati mbalame
yokodwa mu msampha wa mlenje;
msampha wathyoka,
ndipo ife tapulumuka.
8 Thandizo lathu lili m'dzina la Yehova
wolenga kumwamba ndi dziko lapansi.

# Salimo 125

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Amene amadalira Yehova ali ngati phiri la Ziyoni,
limene silingagwedezeke koma ndi lokhala mpaka muyaya.
2 Monga mapiri azungulira Yerusalemu,
momwemonso Yehova azungulira anthu ake

kuyambira tsopano mpaka muyaya.

3 Ndodo yaufumu ya anthu oyipa sidzakhala
pa dziko limene lapatsidwa kwa anthu olungama,
kuti anthu olungamawo
angachite nawonso zoyipa.

4 Yehova chitirani zabwino amene ndi abwino,
amene ndi olungama mtima
5 Koma amene amatembenukira ku njira zokhotakhota,
Yehova adzawachotsa pamodzi ndi anthu ochita zoyipa.

Mtendere ukhale pa Israeli.

# Salimo 126

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Yehova atabwezera akapolo ku Ziyoni,
tinali ngati amene akulota.
2 Pakamwa pathu panadzaza ndi kuseka;
malilime athu ndi nyimbo zachimwemwe.
Pamenepo kunanenedwa pakati pa anthu kuti,
"Yehova wawachitira zinthu zazikulu."
3 Yehova watichitira zinthu zazikulu,
ndipo tadzazidwa ndi chimwemwe.

4 Tibwezereni madalitso athu, Inu Yehova,
monga mitsinje ya ku Negevi.
5 Iwo amene amafesa akulira,
adzakolola akuyimba nyimbo zachimwemwe.
6 Iye amene amayendayenda nalira,
atanyamula mbewu yokafesa,
adzabwerera akuyimba nyimbo zachimwemwe,
atanyamula mitolo yake.

# Salimo 127

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu. Salimo la Solomoni.
1 Yehova akapanda kumanga nyumba,
omanga nyumbayo agwira ntchito pachabe.
Yehova akapanda kulondera mzinda,
mlonda akanangolondera pachabe.
2 Mumangodzivuta n'kulawirira mmamawa
ndi kusagona msanga madzulo,
kuvutikira chakudya choti mudye,
pakuti Iye amapereka tulo kwa amene amawakonda.

3 Ana ndiye cholowa chochokera kwa Yehova,
ana ndi mphotho yochokera kwa Iye.
4 Ana a pa unyamata ali ngati mivi m'manja
mwa munthu wankhondo.
5 Wodala munthu
amene motengera mivi mwake mwadzaza.
Iwo sadzachititsidwa manyazi

pamene alimbana ndi adani awo pa zipata.

# Salimo 128

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Odala ndi onse amene amaopa Yehova,
amene amayenda m'njira zake.
2 Udzadya chipatso cha ntchito yako;
madalitso ndi chuma zidzakhala zako.
3 Mkazi wako adzakhala ngati mpesa wobereka
m'kati mwa nyumba yako;
ana ako adzakhala ngati mphukira za mitengo ya olivi
kuzungulira tebulo lako.
4 Ameneyu ndiye munthu wodalitsidwa
amene amaopa Yehova.

5 Yehova akudalitse kuchokera m'Ziyoni
masiku onse a moyo wako;
uwone zokoma za Yerusalemu,
6 ndipo ukhale ndi moyo kuti udzaone zidzukulu zako.

Mtendere ukhale ndi Israeli.

# Salimo 129

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 "Andizunza kwambiri kuyambira ubwana wanga,"
anene tsono Israeli;
2 "Andizunza kwambiri kuyambira ubwana wanga,
koma sanandipambane.
3 Anthu otipula analima pa msana panga
ndipo anapangapo mizere yayitali:
4 Koma Yehova ndi wolungama;
Iye wandimasula ku zingwe za anthu oyipa."

5 Onse amene amadana ndi Ziyoni
abwezedwe pambuyo mwamanyazi.
6 Akhale ngati udzu womera pa denga la nyumba,
umene umafota usanakule;
7 sungadzaze manja a owumweta
kapena manja a omanga mitolo.
8 Odutsa pafupi asanene kuti,
"Dalitso la Yehova lili pa inu;
tikukudalitsani m'dzina la Yehova."

# Salimo 130

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Ndikulirira kwa Inu Yehova ndili m'dzenje lozama;
2 Ambuye imvani mawu anga.
Makutu anu akhale tcheru kumva
kupempha chifundo kwanga.

3 Inu Yehova, mukanamawerengera machimo,
Inu Yehova, akanayima chilili ndani wopanda mlandu?

4 Koma kwa Inu kuli chikhululukiro;
n'chifukwa chake mumaopedwa.

5 Ndimayembekezera Yehova, moyo wanga umayembekezera,
ndipo ndimakhulupirira mawu ake.
6 Moyo wanga umayembekezera Ambuye,
kupambana momwe alonda amayembekezera mmawa,
inde, kupambana momwe alonda amayembekezera mmawa,

7 Yembekeza Yehova, iwe Israeli,
pakuti Yehova ali ndi chikondi chosasinthika
ndipo alinso ndi chipulumutso chochuluka.
8 Iye mwini adzawombola Israeli
ku machimo ake onse.

# Salimo 131

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu. Salimo la Davide.
1 Inu Yehova, mtima wanga siwodzikuza,
maso anga siwonyada;
sinditengeteka mtima
ndi zinthu zapamwamba ndi zodabwitsa.
2 Koma moyo wanga ndawutontholetsa
ndi kuwukhalitsa chete ngati mwana amene amayi ake amuletsa kuyamwa,
moyo wanga m'kati mwanga uli ngati mwana amene amuletsa kuyamwa.

3 Yembekeza Yehova, iwe Israeli,
kuyambira tsopano mpaka muyaya.

# Salimo 132

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Inu Yehova, kumbukirani Davide
ndi mavuto onse anapirira.

2 Iye analumbira kwa Yehova
ndi kulonjeza kwa Wamphamvu wa Yakobo kuti,
3 "Sindidzalowa m'nyumba mwanga
kapena kugona pa bedi langa:
4 sindidzalola kuti maso anga agone,
kapena zikope zanga ziwodzere,
5 mpaka nditamupezera malo Yehova,
malo okhala a Wamphamvu wa Yakobo."

6 Zoonadi, tinamva za Bokosi la Chipangano ku Efurata,
tinalipeza m'minda ya ku Yaara:
7 "Tiyeni tipite ku malo ake okhalamo;
tiyeni tikamulambire pa mapazi ake.
8 'Dzukani Yehova, ndipo bwerani ku malo anu opumulira,
Inuyo ndi Bokosi la Chipangano limene limafanizira mphamvu zanu.
9 Ansembe anu avekedwe chilungamo;
anthu anu oyera mtima ayimbe nyimbo mwachimwemwe.' "

10 Chifukwa cha Davide mtumiki wanu,
musakane wodzozedwa wanu.

11 Yehova analumbira kwa Davide,
lumbiro lotsimikizika kuti Iye sadzasintha:
"Mmodzi wa ana ako
ndidzamuyika pa mpando waufumu;
12 ngati ana ako azisunga pangano langa
ndi malamulo amene ndiwaphunzitsa,
pamenepo ana awo adzakhala pa mpando
wako waufumu kwamuyaya ndi muyaya."

13 Pakuti Yehova wasankha Ziyoni,
Iye wakhumba kuti akhale malo ake okhalamo:
14 "Awa ndi malo anga opumapo ku nthawi za nthawi;
ndidzakhala pano pa mpando waufumu, pakuti ndakhumba zimenezi.
15 Ndidzadalitsa mzindawu ndi zinthu zambiri;
anthu ake osauka ndidzawakhutitsa ndi chakudya.
16 Ndidzaveka ansembe ake chipulumutso,
ndipo anthu ake oyera mtima adzayimba nthawi zonse nyimbo zachimwemwe.

17 "Pano ndidzachulukitsa mphamvu za Davide
ndi kuyikapo nyale ya wodzozedwa wanga.
18 Ndidzaveka adani ake manyazi,
koma chipewa chaufumu pamutu pake chidzakhala chowala."

# Salimo 133

Salimo la Davide. Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Onani, n'kokoma ndi kokondweretsa ndithu
pamene abale akhala pamodzi mwachiyanjano!
2 Zili ngati mafuta amtengowapatali othiridwa pa mutu,
otsikira ku ndevu,
ku ndevu za Aaroni,
oyenderera mpaka m'khosi mwa mkanjo wake.
3 Zili ngati mame a ku Heremoni
otsikira pa Phiri la Ziyoni.
Pakuti pamenepo Yehova amaperekapo dalitso,
ndiwo moyo wamuyaya.

# Salimo 134

Nyimbo yoyimba pokwera ku Yerusalemu.
1 Bwerani, mutamande Yehova, inu atumiki onse a Yehova,
amene mumatumikira usiku m'nyumba ya Yehova.
2 Kwezani manja anu m'malo opatulika
ndipo mutamande Yehova.

3 Yehova wolenga kumwamba ndi dziko lapansi,
akudalitseni kuchokera m'Ziyoni.

# Salimo 135

1 Tamandani Yehova.

Tamandani dzina la Yehova;
mutamandeni, inu atumiki a Yehova,
2 amene mumatumikira m'nyumba ya Yehova,
m'mabwalo a nyumba ya Mulungu wathu.

3 Tamandani Yehova, pakuti Yehova ndi wabwino;
imbani nyimbo zotamanda dzina lake, pakuti n'kokoma kutero,
4 Pakuti Yehova wasankha Yakobo kuti akhale wake,
Israeli kuti akhale chuma chake chapamtima.

5 Ndikudziwa kuti Yehova ndi wamkulu,
kuti Ambuye athu ndi wamkulu kuposa milungu yonse.
6 Yehova amachita chilichonse chimene chimamukomera,
kumwamba ndi dziko lapansi,
ku nyanja zazikulu ndi ku malo ake onse akuya.
7 Iye amatulutsa mitambo kuchokera ku malekezero a dziko lapansi,
amatumiza zing'aning'ani pamodzi ndi mvula
ndipo amatulutsa mphepo ku malo ake osungiramo.

8 Anakantha ana oyamba kubadwa a Igupto,
ana oyamba kubadwa a anthu ndi nyama.
9 Iye anatumiza zizindikiro zozizwitsa ndi zodabwitsa pakati pako, iwe Igupto,
kutsutsana ndi Farao pamodzi ndi atumiki ake onse.
10 Iye anakantha mitundu yambiri ya anthu
ndi kupha mafumu amphamvu:
11 Sihoni mfumu ya Aamori,
Ogi mfumu ya Basani,
ndi maufumu onse a ku Kanaani;
12 ndipo anapereka dziko lawo ngati cholowa,
cholowa cha anthu ake Aisraeli.

13 Dzina lanu, Inu Yehova, ndi losatha mpaka muyaya,
mbiri yanu, Inu Yehova, idziwika mibado yonse.
14 Pakuti Yehova adzaonetsa kuti anthu ake ngosalakwa,
ndipo adzachitira chifundo atumiki ake.

15 Mafano a mitundu ya anthu ndi siliva ndi golide,
opangidwa ndi manja a anthu.
16 Pakamwa ali napo koma sayankhula
maso ali nawo, koma sapenya;
17 makutu ali nawo, koma sakumva
ndipo m'kamwa mwawo mulibe mpweya uliwonse.
18 Iwo amene amapanga mafanowo adzakhala ngati mafanowo,
chimodzimodzinso iwo amene amadalira mafanowo.

19 Inu nyumba ya Israeli, tamandani Yehova;
inu nyumba ya Aaroni, tamandani Yehova;
20 Inu nyumba ya Levi, tamandani Yehova;
Inu amene mumaopa Iye, tamandani Yehova.
21 Wodalitsika ndi Yehova kuchokera m'Ziyoni,
amene amakhala mu Yerusalemu.

Tamandani Yehova.

# Salimo 136

1 Yamikani Yehova chifukwa ndi wabwino.
Pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
2 Yamikani Mulungu wa milungu.
Pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
3 Yamikani Ambuye wa ambuye,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.

4 Iye yekhayo amene amachita zodabwitsa zazikulu,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
5 Amene mwachidziwitso chake anapanga mayiko akumwamba,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
6 Amene anayala dziko lapansi pamwamba pa madzi,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
7 Amene anapanga miyuni ikuluikulu,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
8 Dzuwa lilamulire usana,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
9 Mwezi ndi nyenyezi zilamulire usiku,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.

10 Amene anakantha ana woyamba kubadwa a Igupto,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
11 Natulutsa Israeli pakati pawo,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
12 Ndi dzanja lamphamvu ndi mkono wotambasuka,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.

13 Amene anagawa Nyanja Yofiira pakati,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
14 Nadutsitsa Israeli pakati pa nyanjayo,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
15 Koma anakokolola Farao ndi ankhondo ake m'Nyanja Yofiira,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.

16 Amene anatsogolera anthu ake m'chipululu
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
17 Amene anakantha mafumu akuluakulu,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
18 Napha mafumu amphamvu,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
19 Siloni mfumu ya Aamori,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
20 Ogi mfumu ya Basani,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
21 Napereka dziko lawo ngati cholowa,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
22 Cholowa cha mtumiki wake Israeli;
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.

23 Amene anatikumbukira ife anthu opeputsidwa,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
24 Amene anatimasula kwa adani athu,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.
25 Amene amapereka chakudya kwa cholengedwa chilichonse,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.

26 Yamikani Mulungu wakumwamba,
pakuti chikondi chake chosasinthika n'chamuyaya.

# Salimo 137

1 M'mbali mwa mitsinje ya ku Babuloni tinakhala pansi ndi kulira
pamene tinakumbukira Ziyoni.
2 Kumeneko, pa mitengo ya misondozi
tinapachika apangwe athu,
3 pakuti anthu otigwira ukapolo anatipempha kuti tiyimbe nyimbo.
Otizunza athu anafuna nyimbo zachisangalalo;
iwo anati, "Tiyimbireni imodzi mwa nyimbo za ku Ziyoni!"

4 Tingayimbe bwanji nyimbo za Yehova
m'dziko lachilendo?
5 Ndikakuyiwala iwe Yerusalemu,
dzanja langa lamanja liyiwale luso lake.
6 Lilime langa limamatire ku nkhama za m'kamwa mwanga
ndikapanda kukukumbukira iwe Yerusalemu,
ngati sindiyesa iwe
chimwemwe changa chachikulu.

7 Kumbukirani, Inu Yehova, zimene Aedomu anachita
pa tsiku limene Yerusalemu anagonja.
Iwowo anafuwula kuti, "Mugwetseni pansi, mugwetseni pansi
mpaka pa maziko ake!"

8 Iwe mwana wa mkazi wa Babuloni, woyenera kuwonongedwa,
wodalitsika ndi yemwe adzakubwezera
pa zimene watichitira.
9 Amene adzagwira makanda ako
ndi kuwakankhanthitsa pa miyala.

# Salimo 138

Salimo la Davide.
1 Ndidzakuyamikani Yehova ndi mtima wanga wonse;
ndidzayimba nyimbo zokutamandani pamaso pa "milungu."
2 Ndidzagwada kuyang'ana ku Nyumba yanu yoyera
ndipo ndidzayamika dzina lanu
chifukwa cha chikondi chanu ndi kukhulupirika kwanu,
pakuti Inu mwakuza dzina lanu ndi mawu anu
kupambana zinthu zonse.
3 Pamene ndinayitana, munandiyankha;
munandisandutsa wamphamvu ndi wolimba mtima.

4 Mafumu onse a dziko lapansi akuyamikeni Yehova,

pamene amva mawu a pakamwa panu.
5 Iwo ayimbe za njira za Yehova,
pakuti ulemerero wa Yehova ndi waukulu.

6 Ngakhale kuti Yehova ngokwezeka, amasamalira odzichepetsa,
koma anthu onyada amawadziwira chapatali.
7 Ngakhale ndiyende pakati pa masautso,
mumasunga moyo wanga;
mumatambasula dzanja lanu kutsutsana ndi mkwiyo wa adani anga,
mumandipulumutsa ndi dzanja lanu lamanja.
8 Yehova adzakwaniritsa cholinga chake pa ine;
chikondi chanu chosasinthika Yehova, ndi chosatha
musasiye ntchito ya manja anu.

# Salimo 139

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Inu Yehova, mwandisanthula
ndipo mukundidziwa.
2 Inu mumadziwa pamene ndikhala pansi ndi pamene ndidzuka;
mumazindikira maganizo anga muli kutali.
3 Mumapenyetsetsa pamene ndikutuluka ndi kugona kwanga;
mumadziwa njira zanga zonse.
4 Mawu asanatuluke pa lilime langa
mumawadziwa bwinobwino, Inu Yehova.

5 Mumandizinga kumbuyo ndi kutsogolo komwe;
mwasanjika dzanja lanu pa ine.
6 Nzeru zimenezi ndi zopitirira nzeru zanga,
ndi zapamwamba kuti ine ndizipeze.

7 Kodi ndingapite kuti kufuna kuzemba Mzimu wanu?
Kodi ndingathawire kuti kuchoka pamaso panu?
8 Ndikakwera kumwamba, Inu muli komweko;
ndikakagona ku malo a anthu akufa, Inu muli komweko.
9 Ngati ndiwulukira kotulukira dzuwa,
ngati ndikakhala ku malekezero a nyanja,
10 kumenekonso dzanja lanu lidzanditsogolera,
dzanja lanu lamanja lidzandigwiriziza.

11 Ndikanena kuti, "Zoonadi, mdima udzandibisa ndithu
ndipo kuwunika kukhale mdima mondizungulira,"
12 komabe mdimawo sudzakhala mdima kwa Inu;
usiku udzawala ngati masana,
pakuti mdima uli ngati kuwunika kwa Inu.

13 Pakuti Inu munalenga za m'kati mwanga;
munandiwumba pamodzi m'mimba mwa amayi anga.
14 Ndimakuyamikani chifukwa ndinapangidwa mochititsa mantha ndi modabwitsa;
ntchito zanu ndi zodabwitsa,
zimenezi ndimazidziwa bwino lomwe.
15 Mapangidwe anga sanabisike pamaso panu

pamene ndimapangidwa m'malo achinsinsi,
pamene ndinkawumbidwa mwaluso m'mimba ya amayi anga.
16 Maso anu anaona thupi langa lisanawumbidwe.
Masiku onse amene anapatsidwa kwa ine, analembedwa m'buku lanu
asanayambe n'kuwerengedwa komwe.

17 Zolingalira zanu pa ine ndi zamtengowapatali, Inu Mulungu,
ndi zosawerengeka ndithu!
18 Ndikanaziwerenga,
zikanakhala zochuluka kuposa mchenga;
pamene ndadzuka, ndili nanube.

19 Ndi bwino mukanangopha anthu oyipa, Inu Mulungu!
Chokereni inu anthu owononga anzanu!
20 Amayankhula za Inu ndi zolinga zoyipa;
adani anu amagwiritsa ntchito dzina lanu molakwika.
21 Kodi ine sindidana nawo amene amakudani, Inu Yehova?
Kodi sindinyansidwa nawo amene amakuwukirani?
22 Ndimadana nawo kwathunthu;
ndi adani anga.

23 Santhuleni, Inu Mulungu ndipo mudziwe mtima wanga;
Yeseni ndipo mudziwe zolingalira zanga.
24 Onani ngati muli mayendedwe aliwonse oyipa mwa ine,
ndipo munditsogolere m'njira yanu yamuyaya.

# Salimo 140

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Salimo la Davide.
1 Landitseni Yehova kwa anthu oyipa;
tetezeni kwa anthu ankhanza,
2 amene mu mtima mwawo amakonza zinthu zoyipa
ndi kuyambitsa nkhondo tsiku lililonse.
3 Iwo amanola malilime awo kukhala akuthwa ngati a njoka;
pa milomo yawo pali ululu wa mamba.
Sela

4 Tetezeni Inu Yehova, kwa anthu oyipa;
tchinjirizeni kwa anthu ankhanza
amene amakonza zokola mapazi anga.
5 Anthu odzikuza anditchera msampha mobisika;
iwo atchera zingwe za maukonde awo
ndipo anditchera misampha pa njira yanga.
Sela

6 Inu Yehova, ine ndikuti, "Ndinu Mulungu wanga."
Imvani kupempha kwanga Yehova.
7 Inu Ambuye Wamphamvuzonse, Mpulumutsi wanga wamphamvu,
mumateteza mutu wanga tsiku lankhondo.
8 Musawapatse anthu oyipa zokhumba zawo, Inu Yehova;
musalole kuti zokonza zawo zitheke,
mwina iwo adzayamba kunyada.
Sela

9 Mitu ya amene andizungulira
iphimbidwe ndi masautso amene milomo yawo yayambitsa.
10 Makala amoto agwere pa iwo;
aponyedwe pa moto,
m'maenje amatope, asatulukemonso.
11 Musalole kuti anthu achipongwe akhazikike m'dziko;
choyipa chilondole anthu ankhanza.

12 Ndikudziwa kuti Yehova amapereka chiweruzo cholungama kwa anthu osauka,
ndipo amateteza zolinga za anthu osowa.
13 Zoonadi anthu olungama adzatamanda dzina lanu,
ndipo anthu owongoka mtima adzakhala pamaso panu.

# Salimo 141

Salimo la Davide.
1 Inu Yehova ndikukuyitanani; bwerani msanga kwa ine.
Imvani mawu anga pamene ndiyitana Inu.
2 Pemphero langa lifike kwa Inu ngati lubani;
kukweza manja kwanga kukhale ngati nsembe yamadzulo.

3 Yehova ikani mlonda pakamwa panga;
londerani khomo la pa milomo yanga.
4 Musalole kuti mtima wanga ukokedwere ku zoyipa;
kuchita ntchito zonyansa
pamodzi ndi anthu amene amachita zoyipa;
musalole kuti ndidye nawo zokoma zawo.

5 Munthu wolungama andikanthe, chimenecho ndiye chifundo;
andidzudzule ndiye mafuta pa mutu wanga.
Mutu wanga sudzakana zimenezi.

Komabe pemphero langa nthawi zonse ndi lotsutsana ndi ntchito za anthu ochita zoyipa.
6 Olamulira awo adzaponyedwa pansi kuchokera pa malo okwera kwambiri,
ndipo anthu oyipa adzaphunzira kuti mawu anga anayankhulidwa bwino.
7 Iwo adzati, "Monga momwe nkhuni zimamwazikira akaziwaza,
ndi momwenso mafupa athu amwazikira pa khomo la manda."

8 Koma maso anga akupenyetsetsa Inu Ambuye Wamphamvuzonse;
ndimathawira kwa Inu, musandipereke ku imfa.
9 Mundipulumutse ku misampha imene anditchera,
ku makhwekhwe amene anthu oyipa andikonzera.
10 Anthu oyipa akodwe m'maukonde awo,
mpaka ine nditadutsa mwamtendere.

# Salimo 142

Ndakatulo ya Davide, pamene iyeyo anali m'phanga. Pemphero.
1 Ndikulirira Yehova mofuwula;
ndikukweza mawu anga kwa Yehova kupempha chifundo.

2 Ndikukhuthula madandawulo anga pamaso pake;
ndikufotokoza za masautso anga pamaso pake.

3 Pamene mzimu wanga walefuka m'kati mwanga,
ndinu amene mudziwa njira yanga.
M'njira imene ndimayendamo
anthu anditchera msampha mobisa.
4 Yang'anani kumanja kwanga ndipo onani;
palibe amene akukhudzika nane.
Ndilibe pothawira;
palibe amene amasamala za moyo wanga.

5 Ndilirira Inu Yehova;
ndikuti, "Ndinu pothawirapo panga,
gawo langa m'dziko la anthu amoyo."
6 Mverani kulira kwanga
pakuti ndathedwa nzeru;
pulumutseni kwa amene akundithamangitsa
pakuti ndi amphamvu kuposa ine.
7 Tulutseni m'ndende yanga
kuti nditamande dzina lanu.

Ndipo anthu olungama adzandizungulira
chifukwa cha zabwino zanu pa ine.

## Salimo 143

Salimo la Davide.
1 Yehova imvani pemphero langa,
mvetserani kulira kwanga kopempha chifundo;
mwa kukhulupirika kwanu ndi chilungamo chanu
bwerani kudzandithandiza.
2 Musazenge mlandu mtumiki wanu,
pakuti palibe munthu wamoyo amene ndi wolungama pamaso panu.

3 Mdani akundithamangitsa,
iye wandipondereza pansi;
wachititsa kuti ndikhale mu mdima
ngati munthu amene anafa kale.
4 Choncho mzimu wanga ukufowoka m'kati mwanga;
m'kati mwanga, mtima wanga uli ndi nkhawa.

5 Ndimakumbukira masiku amakedzana;
ndimalingalira za ntchito yanu yonse,
ndimaganizira zimene manja anu anachita.
6 Ndatambalitsa manja anga kwa Inu;
moyo wanga uli ndi ludzu lofuna Inu monga nthaka yowuma.
Sela

7 Yehova ndiyankheni msanga;
mzimu wanga ukufowoka.
Musandibisire nkhope yanu,
mwina ndidzakhala ngati iwo amene atsikira ku dzenje.

8 Lolani kuti mmawa ubweretse mawu achikondi chanu chosasinthika,
pakuti ine ndimadalira Inu.
Mundisonyeze njira yoti ndiyendemo,
pakuti kwa Inu nditukulira moyo wanga.
9 Pulumutseni kwa adani anga, Inu Yehova,
pakuti ndimabisala mwa Inu.
10 Phunzitseni kuchita chifuniro chanu,
popeza ndinu Mulungu wanga;
Mzimu wanu wabwino unditsogolere
pa njira yanu yosalala.

11 Sungani moyo wanga Inu Yehova chifukwa cha dzina lanu;
mwa chilungamo chanu tulutseni m'masautso anga.
12 Mwa chikondi chanu chosasinthika khalitsani chete adani anga;
wonongani adani anga,
pakuti ndine mtumiki wanu.

# Salimo 144

Salimo la Davide.
1 Atamandike Yehova Thanthwe langa,
amene amaphunzitsa manja anga kuchita nkhondo;
zala zanga kumenya nkhondo.
2 Iye ndiye Mulungu wanga wachikondi ndi malo anga otetezedwa,
linga langa ndi mpulumutsi wanga,
chishango changa mmene ine ndimathawiramo,
amene amagonjetsa mitundu ya anthu pansi panga.

3 Inu Yehova, munthu n'chiyani kuti mumamusamalira,
mwana wa munthu kuti muzimuganizira?
4 Munthu ali ngati mpweya;
masiku ake ali ngati mthunzi wosakhalitsa.

5 Ng'ambani mayiko akumwamba, Inu Yehova, ndipo tsikani pansi;
khudzani mapiri kuti atulutse utsi.
6 Tumizani zing'aning'ani ndi kubalalitsa adani;
ponyani mivi yanu ndi kuwathamangitsa.
7 Tambasulani dzanja lanu kuchokera kumwamba;
landitseni ndi kundipulumutsa,
ku madzi amphamvu,
m'manja mwa anthu achilendo,
8 amene pakamwa pawo ndi podzala ndi mabodza,
amene dzanja lawo lamanja ndi lachinyengo.

9 Ndidzakuyimbirani nyimbo yatsopano Inu Mulungu;
ndidzakuyimbirani nyimbo pa zeze wa nsambo khumi,
10 kwa Iye amene amapambanitsa mafumu,
amene amapulumutsa Davide mtumiki wake ku lupanga loopsa.

11 Landitseni ndi kundipulumutsa,
m'manja mwa anthu achilendo,
amene pakamwa pawo ndi podzaza ndi mabodza,
amene dzanja lawo lamanja ndi lachinyengo.

12 Ndipo ana aamuna pa chinyamata chawo
adzakhala ngati mbewu yosamalidwa bwino,
ana athu aakazi adzakhala ngati zipilala
zosemedwa bwino, zokongoletsera nyumba yaufumu.
13 Nkhokwe zathu zidzakhala zodzaza
ndi zokolola za mtundu uliwonse.
Nkhosa zathu zidzaswana miyandamiyanda
pa mabusa athu.
14 Ng'ombe zathu zidzanyamula katundu wolemera.
Sipadzakhala ming'alu pa makoma,
sipadzakhalanso kupita ku ukapolo,
m'misewu mwathu simudzakhala kulira chifukwa cha mavuto.

15 Odala anthu amene adzalandira madalitso awa;
odala anthu amene Mulungu wawo ndi Yehova.

# Salimo 145

Salimo la matamando la Davide.
1 Ndidzakukwezani Mulungu wanga, Mfumu yanga;
ndidzatamanda dzina lanu ku nthawi za nthawi.
2 Ndidzakutamandani tsiku ndi tsiku
ndi kulemekeza dzina lanu ku nthawi za nthawi.

3 Yehova ndi wamkulu ndi woyenera matamando onse;
ukulu wake palibe angawumvetsetse.
4 M'bado wina udzayamikira ntchito yanu kwa m'bado wina;
Iwo adzafotokoza za machitidwe anu amphamvu.
5 Adzayankhula ulemerero wokongola waufumu wanu,
ndipo ine ndidzalingalira za ntchito zanu zodabwitsa.
6 Iwo adzafotokoza za mphamvu ya ntchito zanu zoopsa kwambiri,
ndipo ine ndidzalengeza za ntchito zanu zazikulu.
7 Adzakondwerera kuchuluka kwa ubwino wanu,
ndi kuyimba mwachimwemwe za chilungamo chanu.

8 Yehova ndi wokoma mtima ndi wachifundo,
wosakwiya msanga ndi wodzaza ndi chikondi chosasinthika.
9 Yehova ndi wabwino kwa onse;
amachitira chifundo zonse zimene anazipanga.
10 Zonse zimene munazipanga zidzakutamandani, Inu Yehova;
oyera mtima adzakulemekezani.
11 Iwo adzafotokoza za ulemerero wa ufumu wanu
ndi kuyankhula za mphamvu yanu,
12 kuti anthu onse adziwe za machitidwe anu amphamvu
ndi ulemerero wokongola wa ufumu wanu.
13 Ufumu wanu ndi ufumu wamuyaya,
ndipo ulamuliro wanu ndi wosatha pa mibado yonse.

Yehova ndi wokhulupirika pa malonjezo ake onse
ndi wokonda zonse zimene Iye anazipanga.
14 Yehova amagwiriziza onse amene akugwa
ndipo amakweza onse otsitsidwa.
15 Maso a onse amayang'ana kwa Inu,

ndipo Inu mumawapatsa chakudya chawo pa nthawi yoyenera.
16 Mumatsekula dzanja lanu
ndi kukwaniritsa zokhumba za chamoyo chilichonse.

17 Yehova ndi wolungama m'njira zake zonse,
ndi wokonda zonse zimene anazipanga.
18 Yehova ali pafupi ndi onse amene amamuyitana,
onse amene amamuyitana Iye m'choonadi.
19 Iye amakwaniritsa zokhumba za iwo amene amamuopa;
amamva kulira kwawo ndi kuwapulumutsa.
20 Yehova amayang'ana onse amene amamukonda
koma adzawononga anthu onse oyipa.

21 Pakamwa panga padzayankhula zotamanda Yehova.
Cholengedwa chilichonse chitamande dzina lake loyera
ku nthawi za nthawi.

# Salimo 146

1 Tamandani Yehova.

Tamanda Yehova, iwe moyo wanga.
2 Ndidzatamanda Yehova ndi moyo wanga wonse;
ndidzayimba nyimbo zamatamando kwa Mulungu wanga nthawi yonse ya moyo wanga.

3 Musamadalire mafumu,
anthu osakhalitsa, amene sangathe kupulumutsa.
4 Pamene mizimu yawo yachoka, iwo amabwerera ku dothi;
zimene ankafuna kuchita zimatha tsiku lomwelo.

5 Wodala ndi amene thandizo lake ndi
Mulungu wa Yakobo.
6 Wolenga kumwamba ndi dziko lapansi,
nyanja ndi zonse zili m'menemo;
Yehova, amene ndi wokhulupirika kwamuyaya.
7 Iye amachitira chilungamo anthu oponderezedwa
ndipo amapereka chakudya kwa anthu anjala.
Yehova amamasula am'ndende,
8 Yehova amatsekula maso anthu osaona,
Yehova amadzutsa onse amene awerama pansi,
Yehova amakonda anthu olungama.
9 Yehova amasamalira alendo
ndipo amathandiza ana ndi akazi amasiye,
koma amasokoneza njira za anthu oyipa.

10 Yehova ndiye Mfumu mpaka muyaya,
Mulungu wako iwe Ziyoni, pa mibado yonse.

Tamandani Yehova.

# Salimo 147

1 Tamandani Yehova.

N'kwabwino kwambiri kuyimba nyimbo zamatamando kwa Mulungu wathu,
n'kokondweretsa ndi koyenera kumutamanda!

2 Yehova akumanga Yerusalemu;
Iye akusonkhanitsa am'ndende a Israeli.
3 Akutsogolera anthu osweka mtima
ndi kumanga mabala awo.

4 Amadziwa chiwerengero cha nyenyezi,
ndipo iliyonse amayitchula dzina.
5 Yehova ndi wamkulu ndi wamphamvu kwambiri;
nzeru zake zilibe malire.
6 Yehova amagwiriziza anthu odzichepetsa,
koma amagwetsa pansi anthu oyipa.

7 Imbirani Yehova ndi mayamiko;
imbani nyimbo kwa Mulungu ndi pangwe.
8 Iye amaphimba mlengalenga ndi mitambo;
amapereka mvula ku dziko lapansi
ndi kumeretsa udzu m'mapiri.
9 Iye amapereka chakudya kwa ng'ombe
ndi kwa ana a makwangwala pamene akulira chakudya.

10 Chikondwerero chake sichili m'mphamvu za kavalo,
kapena m'miyendo ya anthu amphamvu.
11 Yehova amakondwera ndi amene amamuopa,
amene chiyembekezo chawo chili m'chikondi chake chosasinthika.

12 Lemekeza Yehova, iwe Yerusalemu;
tamanda Mulungu wako, iwe Ziyoni,
13 pakuti Iye amalimbitsa mipiringidzo ya zipata zako
ndi kudalitsa anthu ako mwa iwe.
14 Iye amabweretsa mtendere m'malire mwako
ndi kukukhutitsa ndi ufa wa tirigu wosalala.

15 Iyeyo amapereka lamulo pa dziko lapansi;
mawu ake amayenda mwaliwiro.
16 Amagwetsa chisanu ngati ubweya
ndi kumwaza chipale ngati phulusa.
17 Amagwetsa matalala ngati miyala.
Kodi ndani angathe kupirira kuzizira kwake?
18 Amatumiza mawu ake ndipo chisanucho chimasungunuka;
amawombetsa mphepo ndipo madzi amayenda.

19 Iye anawulula mawu ake kwa Yakobo,
malamulo ake ndi zophunzitsa zake kwa Israeli.
20 Sanachitepo zimenezi kwa mtundu wina uliwonse wa anthu;
anthu enawo sadziwa malamulo ake.

Tamandani Yehova.

# Salimo 148

1 Tamandani Yehova.

Tamandani Yehova, inu a kumwamba,
mutamandeni Iye, inu a mlengalenga.
2 Mutamandeni, inu angelo ake onse,
mutamandeni, mutamandeni, inu zolengedwa za mmwamba.
3 Mutamandeni, inu dzuwa ndi mwezi,
mutamandeni, inu nonse nyenyezi zowala.
4 Mutamandeni, inu thambo la kumwambamwamba
ndi inu madzi a pamwamba pa thambo.
5 Zonse zitamande dzina la Yehova
pakuti Iye analamula ndipo zinalengedwa.
6 Iye anaziyika pa malo ake ku nthawi za nthawi;
analamula ndipo sizidzatha.

7 Tamandani Yehova pa dziko lapansi,
inu zolengedwa zikuluzikulu za m'nyanja, ndi nyanja zonse zakuya,
8 inu zing'aning'ani ndi matalala, chipale ndi mitambo,
mphepo yamkuntho imene imakwaniritsa mawu ake,
9 inu mapiri ndi zitunda zonse,
inu mitengo ya zipatso ndi mikungudza yonse,
10 inu nyama zakuthengo ndi ng'ombe zonse,
inu zolengedwa zing'onozing'ono ndi mbalame zowuluka.
11 Inu mafumu a dziko lapansi ndi anthu a mitundu yonse,
inu akalonga ndi olamulira a dziko lapansi.
12 Inu anyamata ndi anamwali,
inu nkhalamba ndi ana omwe.

13 Onsewo atamande dzina la Yehova
pakuti dzina lake lokha ndi lolemekezeka;
ulemerero wake ndi woopsa pa dziko lapansi pano ndi kumwamba komwe.
14 Iye wakwezera nyanga anthu ake,
matamando a anthu ake onse oyera mtima,
Aisraeli, anthu a pamtima pake.

Tamandani Yehova.

# Salimo 149

1 Tamandani Yehova.

Imbirani Yehova nyimbo yatsopano,
matamando ake mu msonkhano wa oyera mtima.

2 Israeli asangalale mwa mlengi wake;
anthu a ku Ziyoni akondwere mwa Mfumu yawo.
3 Atamande dzina lake povina
ndi kuyimbira Iye nyimbo ndi tambolini ndi pangwe.
4 Pakuti Yehova amakondwera ndi anthu ake;
Iye amaveka chipulumutso odzichepetsa.
5 Oyera mtima asangalale mu ulemu wake

ndi kuyimba mwachimwemwe pa mabedi awo.

6 Matamando a Mulungu akhale pakamwa pawo,
ndi lupanga lakuthwa konsekonse m’manja mwawo,
7 kubwezera chilango anthu a mitundu ina,
ndi kulanga anthu a mitundu yonse,
8 kumanga mafumu awo ndi zingwe,
anthu awo otchuka ndi unyolo wachitsulo,
9 kuchita zimene zinalembedwa zotsutsana nawo
Uwu ndi ulemerero wa oyera mtima ake onse.

Tamandani Yehova.

# Salimo 150

1 Tamandani Yehova.

Tamandani Mulungu m’malo ake opatulika;
mutamandeni ku thambo lake lamphamvu.
2 Mutamandeni chifukwa cha machitidwe ake amphamvu;
mutamandeni chifukwa cha ukulu wake wopambana.
3 Mutamandeni poyimba malipenga,
mutamandeni ndi pangwe ndi zeze.
4 Mutamandeni ndi matambolini ndi kuvina,
mutamandeni ndi zingwe ndi zitoliro.
5 Mutamandeni ndi ziwaya zolira za malipenga,
mutamandeni ndi ziwaya zolira kwambiri.

6 Chamoyo chilichonse chopuma chitamande Yehova.

Tamandani Yehova.

# Miyambo

*Mawu Oyamba: Cholinga ndi Mutu*

1 Iyi ndi miyambi ya Solomoni mwana wa Davide, mfumu ya Israeli:
2 Ndi yothandiza kuti munthu adziwe nzeru ndi malangizo;
kuti amvetse mawu a matanthauzo ozama;
3 kuti alandire malangizo othandiza kuti achite zinthu mwanzeru,
akhale wangwiro, wachilungamo ndiponso wosakondera.
4 Ndi yothandiza munthu wamba kuti aphunzire nzeru za kuchenjera,
achinyamata kudziwa zinthu bwino ndi kulingalira.
5 Munthu wanzeru amvetse bwino miyamboyi kuti awonjezere kuphunzira kwake,
ndi munthu womvetsa zinthu bwino apatepo luso,
6 kuti azimvetsa miyambi ndi mafanizo,
mawu a anthu anzeru ndi mikuluwiko.

7 Kuopa Yehova ndiye chiyambi cha nzeru.
Zitsiru zimanyoza nzeru ndi malangizo.

*Malangizo kuti Asunge Nzeru*

*Malangizo kwa Achinyamata*

8 Mwana wanga, mvera malangizo a abambo ako
ndipo usakane mawu okuwongolera a amayi ako.
9 Ali ngati sangamutu yokongola ya maluwa pamutu pako
ndiponso ali ngati mkanda m'khosi mwako.

10 Mwana wanga, ngati anthu oyipa afuna kukukopa
usamawamvere.
11 Akadzati, "Tiye kuno;
tikabisale kuti tiphe anthu,
tikabisalire anthu osalakwa;
12 tiwameze amoyo ngati manda,
ndi athunthu ngati anthu otsikira m'dzenje.
13 Motero tidzapeza zinthu zosiyanasiyana zamtengowapatali
ndi kudzaza nyumba zathu ndi zolanda;
14 Bwera, chita nafe maere,
ndipo tidzagawana chuma chathu tonse."
15 Mwana wanga, usayende nawo pamodzi,
usatsagane nawo m'njira zawozo.
16 Iwowatu amangofuna zoyipa zokhazokha,
amathamangira kukhetsa magazi.
17 N'kopanda phindu kutchera msampha
mbalame zikuona!
18 Koma anthu amenewa amangobisalira miyoyo yawo yomwe;
amangodzitchera okha msampha!
19 Awa ndiwo mathero a anthu opeza chuma mwankhanza;
chumacho chimapha mwiniwake.

*Chenjezo Pomwe Tikana Nzeru*

20 Nzeru ikufuwula mu msewu,

ikuyankhula mokweza mawu m’misika;
21 ikufuwula pa mphambano ya misewu,
ikuyankhula pa zipata za mzinda kuti,

22 “Kodi inu anthu osachangamukanu, mudzakondwera ndi kusachangamuka mpaka liti?
Nanga anthu onyogodola adzakondabe kunyogodola mpaka liti?
Kapena opusa adzadana ndi nzeru mpaka liti?
23 Tamverani mawu anga a chidzudzulo.
Ine ndikukuwuzani maganizo anga
ndi kukudziwitsani mawu anga.
24 Popeza ndinakuyitananani koma inu munakana kumvera.
Ndinayesa kukuthandizani koma panalibe amene anasamala.
25 Uphungu wanga munawunyoza.
Kudzudzula kwanga simunakusamale.
26 Ndiye inenso ndidzakusekani mukadzakhala m’mavuto;
ndidzakunyogodolani chikadzakugwerani chimene mumachiopacho.
27 Chiwonongeko chikadzakugwerani ngati namondwe,
tsoka likadzakufikirani ngati kamvuluvulu,
mavuto ndi masautso akadzakugwerani.

28 “Tsono mudzandiyitana koma sindidzayankha;
mudzandifunafuna, koma simudzandipeza.
29 Popeza iwo anadana ndi chidziwitso
ndipo sanasankhe kuopa Yehova,
30 popeza iwo sanasamale malangizo anga
ndipo ananyoza chidzudzulo changa.
31 Tsono adzadya zipatso zoyenera mayendedwe awo
ndi kukhuta ndi ntchito zimene anachita kwa ena.
32 Pakuti anthu osachangamuka amaphedwa chifukwa cha kusochera kwawo,
ndipo zitsiru zimadziwononga zokha chifukwa cha mphwayi zawo.
33 Koma aliyense wondimvera adzakhala mwa bata;
adzakhala mosatekeseka posaopa chilichonse.”

# 2

*Ubwino Wanzeru*

1 Mwana wanga, ngati ulandira mawu anga
ndi kusunga malamulo anga mu mtima mwako,
2 ndiponso kutchera khutu lako ku nzeru
ndi kuyikapo mtima pa kumvetsa zinthu;
3 ngati upempha kuti uzindikire zinthu
inde kupempha ndi mtima wonse kuti ukhale womvetsa zinthu,
4 ngati ufunafuna nzeruyo ngati siliva
ndi kuyisakasaka ngati chuma chobisika,
5 ndiye udzamvetsa bwino tanthauzo la kuopa Yehova;
ndipo udzapezanso tanthauzo la kumudziwa Yehova.
6 Pakuti Yehova ndiye amapereka nzeru,
ndipo m’kamwa mwake mumachokera chidziwitso ndi kumvetsa zinthu.

7 Anthu olungama zinthu zimawayendera bwino chifukwa Yehova amakhala nawo.
Paja Yehova ndiye chishango cha amene amayenda mwangwiro,
8 pakuti ndiye mlonda wa njira zolungama.
Iye amasamala mayendedwe a anthu ake okhulupirika.

9 Choncho udzamvetsa tanthauzo la ungwiro, chilungamo,
kusakondera ndi njira iliyonse yabwino.
10 Pakuti nzeru idzalowa mu mtima mwako,
kudziwa zinthu kudzakusangalatsa.
11 Kuganizira bwino za m'tsogolo kudzakusunga;
kumvetsa zinthu bwino kudzakuteteza.

12 Nzeru idzakupulumutsa ku mayendedwe oyipa,
kwa anthu amabodza,
13 amene amasiya njira zolungama
namayenda m'njira zamdima,
14 amene amakondwera pochita zoyipa
namasangalala ndi kuyipa kwa ntchito zawo zonyansa.
15 Amenewa ndi anthu a njira zawo zokhotakhota,
ndipo makhalidwe awo ndi achinyengo.

16 Nzeruyo idzakupulumutsanso kwa mkazi wachigololo;
kwa mkazi wachilendo woyankhula moshashalika,
17 amene wasiya mwamuna wa chitsikana wake
ndi kuyiwala pangano limene anachita pamaso pa Mulungu wake.
18 Pakuti nyumba yake imatsetserekera ku imfa;
njira zake zimamufikitsa ku manda.
19 Opita kwa iye palibe ndi mmodzi yemwe amabwerera
kapena kupezanso njira zamoyo.

20 Choncho iwe uziyenda m'njira za anthu abwino,
uzitsata njira za anthu ochita chilungamo.
21 Pakuti anthu olungama ndiwo ati adzakhale m'dziko
ndipo anthu angwiro ndiwo ati adzakhazikike m'menemo;
22 Koma anthu oyipa adzachotsedwa m'dzikomo,
ndipo anthu onyenga adzachotsedwamo.

# 3

*Phindu Lina la Nzeru*

1 Mwana wanga, usayiwale malangizo anga,
mtima wako usunge malamulo anga.
2 Ukatero zaka za moyo wako zidzachuluka
ndipo udzakhala pa mtendere.

3 Makhalidwe ochitira ena chifundo ndi owonetsa kukhulupirika asakuchokere.
Uwamangirire m'khosi mwako ngati mkanda
ndi kuwalemba pa mtima pako.
4 Ukatero udzapeza kuyanja ndi mbiri yabwino
pamaso pa Mulungu ndi anthu.

5 Uzikhulupirira Yehova ndi mtima wako wonse
ndipo usadalire nzeru zako za kumvetsa zinthu.
6 Pa zochita zako zonse uvomereze kuti Mulungu alipo,
ndipo Iye adzawongola njira zako.

7 Usamadzione ngati wa nzeru.
Uziopa Yehova ndi kupewa zoyipa.
8 Ukatero thupi lako lidzakhala la moyo wabwino
ndi mafupa ako adzakhala olimba.

9 Uzilemekeza Yehova ndi chuma chako chonse;
zokolola zonse zoyamba kucha uzilemekeza nazonso Yehova.
10 Ukatero nkhokwe zako zidzadzaza ndi zinthu zambiri,
ndiponso mitsuko yako idzadzaza ndi vinyo.

11 Mwana wanga usanyoze malangizo a Yehova,
ndipo usayipidwe ndi chidzudzulo chake.
12 Paja Yehova amadzudzula amene amamukonda,
monga abambo achitira mwana amene amakondwera naye.

13 Wodala munthu amene wapeza nzeru,
munthu amene walandira nzeru zomvetsa zinthu,
14 pakuti phindu la nzeru ndi labwino kuposa la siliva,
phindu lakelo ndi labwino kuposanso golide.
15 Nzeru ndi yoposa miyala yamtengowapatali;
ndipo zonse zimene umazikhumba sizingafanane ndi nzeru.
16 M'dzanja lake lamanja muli moyo wautali;
m'dzanja lake lamanzere muli chuma ndi ulemu.
17 Njira zake ndi njira zosangalatsa,
ndipo mu njira zake zonse muli mtendere.
18 Nzeru ili ngati mtengo wopatsa moyo kwa oyigwiritsitsa;
wodala munthu amene amayigwiritsa kwambiri.

19 Yehova anakhazikitsa dziko lapansi pogwiritsa ntchito nzeru.
Anagwiritsanso ntchito nzeru zakudziwa bwino zinthu pamene ankakhazikitsa zakumwamba.
20 Mwa nzeru zake Yehova anatumphutsa madzi kuchokera m'nthaka
ndiponso mitambo inagwetsa mvula.

21 Mwana wanga usunge nzeru yeniyeni ndi khalidwe lomalingarira zinthu bwino.
Zimenezi zisakuchokere.
22 Zimenezi zidzakupatsa moyo,
moyo wake wosangalatsa ndi wabwino ngati mkanda wa m'khosi.
23 Choncho udzayenda pa njira yako mosaopa kanthu,
ndipo phazi lako silidzapunthwa;
24 pamene ugona pansi, sudzachita mantha;
ukadzagona pansi tulo tako tidzakhala tokoma.
25 Usaope tsoka lobwera mwadzidzidzi
kapena chiwonongeko chimene chidzagwera anthu oyipa,
26 pakuti Yehova adzakulimbitsa mtima
ndipo adzasunga phazi lako kuti lisakodwe mu msampha.

27 Usaleke kuchitira zabwino amene ayenera kulandira zabwino,
pamene uli nazo mphamvu zochitira zimenezi.
28 Usanene kwa mnansi wako kuti,
“Pita, uchite kubweranso. Ndidzakupatsa mawa”
pamene uli nazo tsopano.

29 Usamukonzere chiwembu mnansi wako,
amene anakhala nawe pafupi mokudalira.
30 Usakangane ndi munthu wopanda chifukwa
pamene iye sanakuchitire zoyipa.

31 Usachite naye nsanje munthu wachiwawa
kapena kutsanzira khalidwe lake lililonse.
32 Pakuti Yehova amanyansidwa ndi munthu woyipa
koma amayanjana nawo anthu olungama.

33 Yehova amatemberera nyumba ya munthu woyipa,
koma amadalitsa nyumba ya anthu olungama.
34 Anthu onyoza, Iye amawanyoza,
koma amakomera mtima anthu odzichepetsa.
35 Anthu anzeru adzalandira ulemu,
koma zitsiru adzazichititsa manyazi.

# 4

*Nzeru Iposa Zonse*

1 Ananu, mverani malangizo a abambo anu;
tcherani khutu kuti mupeze nzeru zodziwira zinthu.
2 Zimene ndikukuphunzitsani ndi zabwino.
Choncho musasiye malangizo anga.
3 Paja ndinalinso mwana m’nyumba mwa abambo anga;
mwana mmodzi yekha wapamtima pa amayi anga.
4 Ndipo abambo anandiphunzitsa ndi mawu akuti,
“Ugwiritse mawu anga pa mtima pako,
usunge malamulo anga kuti ukhale ndi moyo.
5 Upeze nzeru, upeze nzeru zomvetsa zinthu;
usayiwale mawu anga kapena kutayana nawo.
6 Usasiye nzeru ndipo idzakusunga.
Uziyikonda ndipo idzakuteteza.
7 Fundo yayikulu pa za nzeru ndi iyi: upeze nzeru.
Kaya pali china chilichonse chimene ungapeze, koma upeze nzeru yomvetsa bwino zinthu.
8 Uyilemekeze nzeruyo ndipo idzakukweza;
ikumbatire nzeruyo ndipo idzakupatsa ulemu.
9 Idzayika sangamutu yokongola yamaluwa pamutu pako;
idzakupatsa chipewa chaufumu chaulemu.”

10 Mwana wanga, umvere ndi kuvomereza zimene ndikunena,
ndipo zaka za moyo wako zidzakhala zochuluka.
11 Ndakuphunzitsa njira yake ya nzeru.
Ndakutsogolera m’njira zolungama.
12 Pamene ukuyenda, mapazi ako sadzawombana;

ukamadzathamanga, sudzapunthwa.
13 Ugwiritse zimene ndikukuphunzitsazi osazitaya ayi.
Uwasamale bwino pakuti moyo wako wagona pamenepa.
14 Usayende m'njira za anthu oyipa
kapena kuyenda m'njira ya anthu ochimwa.
15 Pewa njira zawo, usayende m'menemo;
uzilambalala n'kumangopita.
16 Pakuti iwo sagona mpaka atachita zoyipa;
tulo salipeza mpaka atapunthwitsa munthu wina.
17 Paja chakudya chawo ndicho kuchita zoyipa basi
ndipo chakumwa chawo ndi chiwawa.

18 Koma njira ya anthu olungama ili ngati kuwala kwa m'bandakucha
kumene kumanka kuwalirawalira mpaka dzuwa litafika pa mutu.
19 Koma njira ya anthu oyipa ili ngati mdima wandiweyani;
iwo sadziwa chomwe chimawapunthwitsa.

20 Mwana wanga, mvetsetsa zimene ndikunena;
tchera khutu ku mawu anga.
21 Usayiwale malangizo angawa,
koma uwasunge mu mtima mwako.
22 Pakuti amapatsa moyo kwa aliyense amene awapeza
ndipo amachiritsa thupi lake lonse.
23 Ndipotu mtima wako uziwuyang'anira bwino ndithu
pakuti ndiwo magwero a moyo.
24 Usiyiretu kuyankhula zokhotakhota;
ndipo ulekeretu kuyankhula zinthu zonyansa.
25 Maso ako ayang'ane patsogolo;
uziyang'ana kutsogolo molunjika.
26 Uzilingalira bwino kumene kupita mapazi ako
ndipo njira zako zonse zidzakhala zosakayikitsa.
27 Usapatukire kumanja kapena kumanzere;
usapite kumene kuli zoyipa.

# 5

### *Chenjezo kwa Mkazi Wachigololo*

1 Mwana wanga, mvetsera bwino za nzeru zimene ndikukuwuzazi,
tchera khutu ku mawu odziwitsa bwino zinthu ndikukupatsa,
2 kuti uthe kuchita zinthu mochenjera ndi mwanzeru
ndiponso kuti utetezedwe ku mayankhulidwe a mkazi wachilendo.
3 Pakuti mkazi wachigololo ali ndi mawu okoma ngati uchi.
Zoyankhula zake ndi zosalala ngati mafuta,
4 koma kotsirizira kwake ngowawa ngati ndulu;
ngakuthwa ngati lupanga lakuthwa konsekonse.
5 Mapazi ake amatsikira ku imfa;
akamayenda ndiye kuti akupita ku manda.
6 Iye saganizirapo za njira ya moyo;
njira zake ndi zokhotakhota koma iye sadziwa izi.

7 Tsopano ana inu, mundimvere;

musawasiye mawu anga.
8 Uziyenda kutali ndi mkazi wotereyo,
usayandikire khomo la nyumba yake,
9 kuopa kuti ungadzalanditse ulemerero wako kwa anthu ena;
ndi zaka zako kwa anthu ankhanza,
10 kapenanso alendo angadyerere chuma chako
ndi phindu la ntchito yako kulemeretsa anthu ena.
11 Potsiriza pa moyo wako udzabuwula,
thupi lako lonse litatheratu.
12 Ndipo udzati, "Mayo ine, ndinkadana ndi kusunga mwambo!
Mtima wanga unkanyoza chidzudzulo!
13 Sindinamvere aphunzitsi anga
kapena alangizi anga.
14 Ine ndatsala pang'ono kuti ndiwonongeke
pakati pa msonkhano wonse."

15 Imwa madzi a m'chitsime chakochako,
madzi abwino ochokera m'chitsime chako.
16 Kodi akasupe ako azingosefukira m'misewu?
Kodi mitsinje yako izingoyendayenda m'zipata za mzinda?
17 Mitsinjeyo ikhale ya iwe wekha,
osati uyigawireko alendo.
18 Yehova adalitse kasupe wako,
ndipo usangalale ndi mkazi wa unyamata wako.
19 Iye uja ali ngati mbalale yayikazi yokongola ndiponso ngati gwape wa maonekedwe abwino.
Ukhutitsidwe ndi mawere ake nthawi zonse,
ndipo utengeke ndi chikondi chake nthawi zonse.
20 Mwana wanga, n'chifukwa chiyani ukukopeka ndi mkazi wachigololo?
Bwanji ukukumbatira mkazi wachilendo?

21 Pakuti mayendedwe onse a munthu Yehova amawaona,
ndipo Iye amapenyetsetsa njira zake zonse.
22 Ntchito zoyipa za munthu woyipa zimamukola yekha;
zingwe za tchimo lake zimamumanga yekha.
23 Iye adzafa chifukwa chosowa mwambo,
adzasocheretsedwa chifukwa cha uchitsiru wake waukulu.

# 6

*Za Moyo wa Uchitsiru*

1 Mwana wanga, ngati wamuperekera mnansi wako chikole,
ngati walonjeza kumulipirira mlendo,
2 ngati wagwidwa ndi zimene iwe unanena,
wakodwa ndi mawu a m'kamwa mwako.
3 Tsono popeza iwe mwana wanga
wadziponya m'manja mwa mnansi wako, chita izi kuti udzipulumutse:
pita msanga ukamupemphe mnansi wako;
kuti akumasule!
4 Usagone tulo,
usawodzere.
5 Dzipulumutse monga imachitira mphoyo m'dzanja la mlenje,

ndi monga imachitira mbalame mu msampha wa munthu wosaka.

6 Pita kwa nyerere, mlesi iwe;
kaonetsetse njira zake kuti uphunzirepo kanthu!
7 Zilibe mfumu,
zilibe woyang'anira kapena wolamulira,
8 komabe zimasungiratu chakudya chake nthawi ya chilimwe
ndipo zimatuta chakudyacho nthawi yokolola.

9 Kodi uzingogonabe pamenepo mpaka liti mlesi iwe?
Kodi tulo tako tidzatha liti?
10 Ukati ndingogona pang'ono, ndingowodzera pang'ono
ndingopinda manjawa pang'ono kuti ndipumule,
11 umphawi udzakugwira ngati mbala
ndipo usiwa udzafika ngati munthu wachifwamba.

12 Munthu wachabechabe, munthu woyipa,
amangoyendayenda ndi kumayankhula zoyipa,
13 amatsinzinira maso ake,
namakwakwaza mapazi ake
ndi kulozaloza ndi zala zake,
14 amalingalira zoyipa ndi mtima wake wachinyengo
ndipo nthawi zonse amangokhalira kuyambitsa mikangano pakati pa anthu.
15 N'chifukwa chake tsoka lidzamugwera modzidzimutsa;
adzawonongeka msangamsanga popanda chomupulumutsa.

16 Pali zinthu zisanu ndi chimodzi zimene Yehova amadana nazo,
zinthu zisanu ndi ziwiri zimene zimamunyansa:
17 maso onyada,
pakamwa pabodza,
manja akupha munthu wosalakwa,
18 mtima wokonzekera kuchita zoyipa,
mapazi othamangira msanga ku zoyipa,
19 mboni yonama yoyankhula mabodza
komanso munthu amene amayambitsa mikangano pakati pa abale.

*Chenjezo pa za Chigololo*

20 Mwana wanga, usunge malamulo a abambo ako;
ndipo usataye zimene anakuphunzitsa amayi ako.
21 Zimenezi uzimatirire pa mtima pako masiku onse,
uzimangirire m'khosi mwako.
22 Ukamayenda, zidzakulozera njira;
ukugona, zidzakulondera;
ukudzuka, zidzakuyankhula.
23 Paja malamulo awa ali ngati nyale,
malangizowa ali ngati kuwunika,
ndipo chidzudzulo cha mwambo ndiwo
moyo weniweni,
24 kukupulumutsa kwa mkazi wadama,
zimenezi zidzakutchinjiriza kwa mkazi wadama, ndi kukuthandiza kuti usamvere mawu oshashalika a mkazi wachiwerewere.

25 Mu mtima wako usakhumbire kukongola kwake,
asakukope ndi zikope zake,
26 paja mkazi wadama amakusandutsa kukhala ngati nyenyeswa za buledi
ndipo mkazi wa mwini wake amasokonezeratu moyo wako wonse.
27 Kodi munthu angathe kutenga moto
zovala zake osapsa?
28 Kodi munthu angathe kuyenda pa makala amoto
mapazi ake osapserera?
29 Ndizo zimachitikira munthu amene amagonana ndi mkazi wa munthu wina.
Aliyense wokhudza mkazi wotere adzalangidwa.

30 Paja anthu sayinyoza mbala ikaba
chifukwa chakuti ili ndi njala.
31 Komabe ngati mbalayo igwidwa iyenera kulipira kasanu n'kawiri,
ngakhale kulandidwa katundu wa m'nyumba mwake.
32 Munthu wochita chigololo ndi wopanda nzeru.
Wochita zimenezi amangodziwononga yekha.
33 Adzalandira mabala ndi m'nyozo,
ndipo manyazi ake sadzamuchokera.
34 Paja nsanje imachititsa mwini mkaziyo kukalipa,
ndipo sadzachita chifundo pobwezera.
35 Iye savomera dipo lililonse;
sangapepeseke ngakhale umupatse mphatso zochuluka motani.

# 7

*Za Mkazi Wachigololo*

1 Mwana wanga, mvera mawu anga;
usunge bwino malamulo angawa.
2 Utsate malamulo anga ndipo udzakhala ndi moyo;
samala malangizo angawa monga uchitira ndi maso ako.
3 Uchite ngati wawamangirira pa zala zako,
ndiponso ngati kuti wawalemba pa mtima pako.
4 Nzeru uyiwuze kuti, "Iwe ndiwe mlongo wanga,"
ndipo khalidwe lomvetsa bwino zinthu ulitchule kuti, "Bwenzi langa lapamtima."
5 Zidzakuteteza kwa mkazi wachigololo
ndiponso zidzakuthandiza kusamvera mawu oshashalika a mkazi wachilendo.

6 Tsiku lina pa zenera la nyumba yanga
ndinasuzumira pa zenera.
7 Ndinaona pakati pa anthu opusa,
pakati pa anyamata,
mnyamata wina wopanda nzeru.
8 Iye ankayenda njira yodutsa pafupi ndi nyumba ya mkaziyo,
kuyenda molunjika nyumba ya mkaziyo.
9 Inali nthawi yachisisira madzulo,
nthawi ya usiku, kuli mdima.

10 Ndipo mkaziyo anadzakumana naye,

atavala ngati munthu wachiwerewere wa mtima wonyenga.
11 (Mkaziyo ndi wolongololа ndiponso nkhutukumve,
iye ndi wosakhazikika pa khomo.
12 Mwina umupeza pa msewu, mwina umupeza pa msika,
ndipo amadikirira munthu pa mphambano iliyonse).
13 Tsono amagwira mnyamatayo ndi kupsompsona
ndi nkhope yake yopanda manyazi amamuwuza kuti,

14 "Ndinayenera kupereka nsembe zachiyanjano.
Lero ndakwaniritsa malumbiro anga.
15 Choncho ndinabwera kudzakumana nawe;
ndinkakufunafuna ndipo ndakupeza!
16 Pa bedi panga ndayalapo
nsalu zosalala zokongola zochokera ku Igupto.
17 Pa bedi panga ndawazapo zonunkhira
za mure, mafuta onunkhira a aloe ndi sinamoni.
18 Bwera, tiye tikhale malo amodzi kukondwerera chikondi mpaka mmawa;
tiye tisangalatsane mwachikondi!
19 Mwamuna wanga kulibe ku nyumbako;
wapita ulendo wautali:
20 Anatenga thumba la ndalama
ndipo adzabwera ku nyumba mwezi ukakhwima."

21 Ndi mawu ake onyengerera amamukakamiza mnyamatayo;
amukopa ndi mawu ake oshashalika.
22 Nthawi yomweyo chitsiru chimamutsatira mkaziyo
ngati ng'ombe yopita kukaphedwa,
monga momwe mbawala ikodwera mu msampha,
23 mpaka muvi utalasa chiwindi chake,
chimakhala ngati mbalame yothamangira m'khwekhwe,
osadziwa kuti moyo wake uwonongeka.

24 Tsono ana inu, ndimvereni;
mvetsetsani zimene ndikunena.
25 Musatengeke mtima ndi njira za mkazi ameneyu;
musasochere potsata njira zake.
26 Paja iye anagwetsa anthu ambiri;
wapha gulu lalikulu la anthu.
27 Nyumba yake ndi njira yopita ku manda,
yotsikira ku malo a anthu akufa.

# 8

*Nzeru Ikuyitana*

1 Kodi nzeru sikuyitana?
Kodi nzeru yomvetsa zinthu sinakweze mawu ake?
2 Nzeru imayima pa zitunda m'mbali mwa njira,
imayima pa mphambano ya misewu.
3 Imafuwula pafupi ndi zipata zolowera mu mzinda,
pa makomo olowera imafuwula kuti,
4 Inu anthu, ndikuyitana inu;

ndikuyitanatu anthu onse.
5 Inu amene simudziwa kanthunu khalani ochenjera;
inu amene ndi opusa, khalani ndi mtima womvetsa zinthu.
6 Mverani, pakuti ndikukuwuzani zinthu zofunika kwambiri;
ndatsekula pakamwa panga ndipo payankhula zolungama.
7 Pakamwa panga pamayankhula zoona
ndimanyansidwa ndi kuyankhula zoyipa.
8 Mawu onse a pakamwa panga ndi olungama;
m'mawu angawo mulibe zokhotakhota kapena zopotoka.
9 Kwa anthu ozindikira, mawu anga onse ndi woona;
kwa anthu amene ali ndi nzeru zomvetsa zinthu, mawu angawo ndi okhoza.
10 Landirani malangizo anga m'malo mwa siliva,
nzeru zomvetsa zinthu m'malo mwa golide wabwino.
11 Paja nzeru ndi yabwino kwambiri kuposa miyala yamtengowapatali,
ndipo zonse zimene ungazifune sizingafanane ndi nzeru.

12 Ine nzeru, ndimakhala pamodzi ndi kuchenjera.
Ine ndimadziwa zinthu ndiponso ndimalingalira zinthu bwino.
13 Kuopa Yehova ndiko kudana ndi zoyipa.
Ine ndimadana ndi kunyada, kudzitama,
kuchita zoyipa, ndiponso kuyankhula zonyenga.
14 Ndine mwini uphungu ndi maganizo abwino;
ndili ndi nzeru yomvetsa zinthu ndiponso mphamvu.
15 Ndine amene ndimathandiza mafumu kulamulira.
Ndimawathandiza olamulira kukhazikitsa malamulo olungama.
16 Ndine amene ndimathandiza akalonga polamula.
Ndinenso amene ndimathandiza akuluakulu onse kulamulira bwino dziko.
17 Ndimakonda amene amandikonda,
ndipo amene amandifunafuna amandipeza.
18 Ine ndili ndi chuma ndi ulemu,
chuma ndi kupindula pa ntchito kokhazikika.
19 Chipatso changa ndi chabwino kuposa golide, ngakhale golide wosalala;
zimene ine ndimabereka zimaposa siliva wabwino kwambiri.
20 Ndimachita zinthu zolungama.
Ine sindipatuka m'njira za chilungamo.
21 Ndimapereka chuma kwa amene amandikonda
ndi kudzaza nyumba zawo zosungiramo chuma.

22 "Yehova anandilenga ine nzeru monga ntchito yake yoyamba.
Mwa ntchito zake zakalekale yoyamba ndinali ine.
23 Ndinapangidwa kalekalelo,
pachiyambi penipeni dziko lapansi lisanalengedwe.
24 Nyanja, akasupe odzaza ndi madzi,
zonsezi kulibe pamene ine ndinkabadwa.
25 Mapiri asanakhazikitsidwe pa malo awo,
mapiri ang'onoang'ono asanakhalepo, ine ndinali nditabadwa kale,
26 lisanalengedwe dziko lapansi ndi minda yake;
lisanalengedwe dothi loyamba la dziko lapansi.
27 Ine ndinalipo pamene Yehova ankakhazikitsa mlengalenga,
pamene ankalemba malire a nyanja yozama,

28 pamene anakhazikitsa mitambo ya mlengalenga
ndi kukhazikitsa akasupe a madzi ozama,
29 pamene anayikira nyanja malire
kuti madzi asadutse malirewo,
ndiponso pamene ankayika malire a dziko lapansi.
30 Tsono ine ndinali pambali pake ngati mmisiri;
ndikumukondweretsa tsiku ndi tsiku,
kusangalala nthawi zonse pamaso pake.
31 Ndinkasangalala ndi dziko lake lonse
ndiponso kumakondwera nawo anthu onse."

32 "Ndiye tsono ana inu, ndimvereni;
odala anthu amene amasunga njira zanga.
33 Mverani malangizo anga kuti mukhale ndi nzeru;
musanyozere mawu anga.
34 Wodala munthu amene amandimvera,
amene amakhala pa khomo panga tsiku ndi tsiku,
kudikirira pa chitseko changa.
35 Paja aliyense amene apeza ine wapeza moyo
ndipo Yehova amamukomera mtima.
36 Koma amene alephera kundipeza, amadzipweteka yekha;
onse amene amandida amakonda imfa."

# 9

*Za Nzeru ndi Uchitsiru*

1 Nzeru inamanga nyumba yake;
inayimika nsanamira zake zisanu ndi ziwiri.
2 Inapha ziweto zake ndipo yasakaniza vinyo wake;
inasakaniza vinyo wake ndi kuyala tebulo lake.
3 Nzeruyo inatuma adzakazi ake,
kuti akakhale pamwamba penipeni pa mzinda ndi kukalengeza kuti,
4 "Aliyense amene ali munthu wamba, abwere kuno!"
Kwa onse opanda nzeru inkanena kuti,
5 "Bwerani, dzadyeni chakudya changa
ndipo dzamweni vinyo amene ndakonza.
6 Lekani zopusa zanu kuti mukhale ndi moyo;
yendani njira ya nzeru yomvetsa zinthu."

7 Aliyense amene amayesa kukonza munthu wonyoza amadziputira minyozo;
aliyense amene amadzudzula munthu woyipa amadetsa mbiri yake.
8 Usadzudzule munthu wonyoza kuti angadzadane nawe;
dzudzula munthu wanzeru ndipo adzakukonda.
9 Ukalangiza munthu wanzeru ndiye adzapitirira kukhala wanzeru;
ukaphunzitsa munthu wolungama ndiye adzawonjezera kuphunzira kwake.

10 Kuopa Yehova ndiye chiyambi cha nzeru;
kudziwa Woyerayo ndiko kukhala womvetsa bwino zinthu.
11 Chifukwa cha ine nzeru, masiku ako adzachuluka,
ndipo zaka za moyo wako zidzawonjezeredwa.

12 Ngati ndiwe wanzeru, nzeru yakoyo idzakupindulitsa;
ngati ndiwe wonyoza ena, udzavutika wekha.

13 Uchitsiru ndi mkazi waphokoso,
wopulikira ndiponso wosadziwa zinthu.
14 Iye amakhala pa mpando, pa khomo la nyumba yake,
pamalo aatali a mu mzinda,
15 kuti aziyitana anthu ongodutsa,
amene akunka nayenda njira zawo.
16 Amati, "Onse amene ndi anthu wamba abwere kuno,"
ndipo kwa wopanda nzeru amati,
17 "Madzi akuba ndiye amatsekemera;
chakudya chodya mobisa ndi chokoma!"
18 Koma amunawo sadziwa kuti akufa ali kale komweko,
ndi kuti alendo ake alowa kale m'manda akuya.

# 10

*Miyambo ya Solomoni*

1 Miyambo ya Solomoni:
Mwana wanzeru amakondweretsa abambo ake,
koma mwana wopusa amamvetsa amayi ake chisoni.

2 Chuma chochipeza mwachinyengo sichipindulitsa,
koma chilungamo chimapulumutsa ku imfa.

3 Yehova salola kuti munthu wolungama azikhala ndi njala;
koma amalepheretsa zokhumba za anthu oyipa.

4 Wochita zinthu mwaulesi amasauka,
koma wogwira ntchito mwakhama amalemera.

5 Amene amakolola nthawi yachilimwe ndi mwana wanzeru,
koma amene amangogona nthawi yokolola ndi mwana wochititsa manyazi.

6 Madalitso amakhala pa mutu wa munthu wolungama,
koma pakamwa pa munthu woyipa pamaphimba chiwawa.

7 Munthu wolungama anzake adzamukumbukira ngati mdalitso,
koma dzina la munthu woyipa lidzayiwalika.

8 Munthu wa mtima wanzeru amasamala malamulo,
koma chitsiru chomangolongolola chidzawonongeka.

9 Munthu woyenda mwangwiro amayenda mosatekeseka;
koma amene amayenda njira yokhotakhota adzadziwika.

10 Aliyense wotsinzinira maso mwachinyengo amabweretsa mavuto,
koma wodzudzula chitsiru molimba mtima amabweretsa mtendere.

11 Pakamwa pa munthu wolungama ndi kasupe wamoyo,

koma pakamwa pa munthu woyipa pamabisa chiwawa.

12 Udani umawutsa mikangano,
koma chikondi chimaphimba zolakwa zonse.

13 Nzeru imapezeka pa milomo ya munthu wozindikira zinthu,
koma pa msana pa munthu wopanda nzeru sipachoka chikwapu.

14 Anzeru amasunga chidziwitso
koma pakamwa pa chitsiru pamatulutsa zowononga.

15 Chuma cha munthu wolemera
ndiye chitetezo chake; koma umphawi ndiye chiwonongeko cha osauka.

16 Moyo ndiye malipiro a munthu wolungama,
koma phindu la anthu oyipa ndi uchimo ndi imfa.

17 Wosamalira malangizo amayenda m'njira ya moyo,
koma wonyoza chidzudzulo amasochera.

18 Amene amabisa chidani chake ndi munthu wonama,
ndipo amene amafalitsa miseche ndi chitsiru.

19 Mawu akachuluka zolakwa sizisowa,
koma amene amasunga pakamwa pake ndi wanzeru.

20 Mawu a munthu wolungama ali ngati siliva wabwino kwambiri,
koma mtima wa munthu woyipa ndi wopanda phindu.

21 Milomo ya anthu olungama imalimbikitsa ambiri;
koma chitsiru chimafa chifukwa chosowa nzeru.

22 Mdalitso wa Yehova ndiwo umabweretsa chuma,
ntchito za munthu siziwonjezerapo kanthu.

23 Kwa chitsiru kuchita zinthu zoyipa ndiye chinthu chomusangalatsa,
koma kwa munthu womvetsa bwino zinthu nzeru ndiyo imamusangalatsa.

24 Chimene munthu woyipa amachiopa chidzamuchitikira;
chimene munthu wolungama amachilakalaka adzachipeza.

25 Pamene namondwe wawomba, anthu oyipa amachotsedwa,
koma anthu olungama amakhazikika mpaka muyaya.

26 Momwe amakhalira vinyo wosasa m'kamwa ndi momwe umakhalira utsi m'maso,
ndi momwenso amakhalira munthu waulesi kwa amene amutuma.

27 Kuopa Yehova kumatalikitsa moyo;
koma zaka za anthu oyipa zidzafupikitsidwa.

28 Chiyembekezo cha olungama chimapatsa chimwemwe,
koma chiyembekezo cha anthu ochimwa chidzafera m'mazira.

29 Njira za Yehova ndi linga loteteza anthu ochita zabwino,
koma wochita zoyipa adzawonongeka.

30 Munthu wolungama sadzachotsedwa, pamalo pake
koma oyipa sadzakhazikika pa dziko.

31 Pakamwa pa munthu wolungama pamatulutsa za nzeru,
koma lilime lokhota lidzadulidwa.

32 Milomo ya anthu olungama imadziwa zoyenera kuyankhula,
koma pakamwa pa anthu ochimwa pamatulutsa zokhota zokhazokha.

# 11

1 Muyeso wachinyengo Yehova umamunyansa,
koma amakondwera ndi muyeso woyenera.

2 Kunyada kukalowa, pamafikanso manyazi,
koma pamene pali kudzichepetsa pameneponso pali nzeru.

3 Ungwiro wa anthu olungama umawatsogolera,
koma anthu osakhulupirika amawonongeka ndi chinyengo chawo.

4 Chuma sichithandiza pa tsiku lawukali wa Mulungu,
koma chilungamo chimapulumutsa ku imfa.

5 Chilungamo cha anthu angwiro chimawongolera moyo wawo,
koma ntchito zoyipa zimagwetsa mwini wake yemweyo.

6 Chilungamo cha anthu oyera mtima chimawapulumutsa,
koma anthu onyenga adzagwidwa ndi zilakolako zawo zomwe.

7 Pamene munthu woyipa wafa, chiyembekezo chake chimathanso.
Chiyembekezo cha munthu wosalungama chimawonongeka.

8 Munthu wolungama amapulumutsidwa ku mavuto,
koma m'malo mwake amagwa m'mavutomo ndi anthu oyipa.

9 Munthu wosapembedza amawononga mnansi wake ndi pakamwa pake,
koma munthu wolungama amapulumuka chifukwa cha kudziwa zinthu.

10 Anthu olungama zinthu zikamawayendera bwino, mzinda wonse umakondwera,
ndipo oyipa akamawonongeka anthu amafuwula mwachimwemwe.

11 Mzinda umakwezeka chifukwa cha madalitso a anthu oyera mtima,
koma umawonongedwa chifukwa cha pakamwa pa anthu oyipa.

12 Munthu wonyoza mnzake ndi wopanda nzeru,

koma munthu wanzeru zomvetsa zinthu amakhala chete.

13 Amene amanka nachita ukazitape amawulula zinsinsi;
koma munthu wokhulupirika amasunga pakamwa pake.

14 Pakasoweka uphungu mtundu wa anthu umagwa;
koma pakakhala aphungu ambiri pamakhalanso chipulumutso.

15 Woperekera mlendo chikole adzapeza mavuto,
koma wodana ndi za chikole amakhala pa mtendere.

16 Mkazi wodekha amalandira ulemu,
koma amuna ankhanza amangopata chuma.

17 Munthu wachifundo amadzipindulira zabwino
koma munthu wankhanza amadzibweretsera mavuto.

18 Munthu woyipa amalandira malipiro wopanda phindu,
koma wochita chilungamo amakolola mphotho yeniyeni.

19 Munthu wochita za chilungamo amapeza moyo,
koma wothamangira zoyipa adzafa.

20 Yehova amanyansidwa ndi anthu a mtima wokhotakhota
koma amakondwera ndi anthu a makhalidwe angwiro.

21 Zoonadi, anthu oyipa adzalangidwa,
koma anthu olungama adzapulumuka.

22 Monga imaonekera mphete yagolide ikakhala pa mphuno ya nkhumba,
ndi momwenso amaonekera mkazi wokongola wam'kamwa.

23 Zokhumba za anthu olungama zimathera pa zabwino zokhazokha,
koma chiyembekezo cha anthu oyipa chimathera mu ukali wa Mulungu.

24 Munthu wina amapatsako anzake zinthu mwaufulu n'kumangolemererabe;
wina amamana chomwe akanatha kupereka, koma kumanka nasawukabe.

25 Munthu wopereka mowolowamanja adzalemera;
iye amene amathandiza ena iyenso adzathandizidwa.

26 Anthu amatemberera womana anzake chakudya,
koma madalitso amakhala pamutu pa munthu amene amagulitsa chakudyacho.

27 Iye amene amafunafuna zabwino mwakhama amapeza zabwinozo,
koma wofunafuna zoyipa zidzamupeza.

28 Aliyense amene amadalira chuma chake adzafota,

koma wolungama adzaphukira ngati tsamba lobiriwira.

29 Wovutitsa a m'nyumba mwake adzalowa m'mavuto,
ndipo chitsiru chidzakhala kapolo wa munthu wa nzeru.

30 Chipatso cha ntchito zabwino ndi moyo,
ndipo kusatsata malamulo kumawonongetsa moyo.

31 Ngati anthu olungama amalandira mphotho zawo pa dziko lapansi,
kuli bwanji anthu osapembedza ndi ochimwa!

# 12

1 Munthu amene amakonda mwambo amakonda kudziwa zinthu,
koma amene amadana ndi chidzudzulo ndi wopusa.

2 Munthu wabwino amapeza kuyanja pamaso pa Yehova,
koma Yehova amatsutsa munthu wochita chinyengo.

3 Munthu sangakhazikike bwino pochita zoyipa,
koma maziko a anthu olungama sadzatekeseka.

4 Mkazi wakhalidwe labwino ali ngati chipewa chaufumu kwa mwamuna wake,
koma mkazi wochititsa manyazi ali ngati chilonda cha mafinya kwa mwamuna wake.

5 Maganizo a anthu olungama ndi owongoka,
koma malangizo a anthu oyipa ndi achinyengo.

6 Mawu a anthu oyipa ndi ophetsa,
koma mawu a anthu olungama amapulumutsa.

7 Anthu oyipa amagonjetsedwa ndipo amayiwalika,
koma nyumba ya anthu olungama idzakhalabe.

8 Munthu amatamandidwa malinga ndi nzeru zake,
koma anthu amitima yokhota amanyozedwa.

9 N'kwabwino kukhala munthu wonyozeka koma wodzigwirira ntchito n'kukhala ndi zonse zofunika,
kuposa kukhala wodzikuza koma ulibe ndi chakudya chomwe.

10 Munthu wolungama amasamalira moyo wa ziweto zake,
koma chifundo cha munthu woyipa ndi chakhanza.

11 Wolima m'munda mwake mwakhama adzakhala ndi chakudya chochuluka,
koma wotsata zopanda pake alibe nzeru.

12 Munthu woyipa amalakalaka zofunkha za anthu oyipa,
koma mizu ya anthu olungama imabereka zipatso.

13 Munthu woyipa amakodwa mu msampha wa mayankhulidwe ake oyipa;
koma munthu wolungama amatuluka m'mavuto.

14 Munthu amakhala ndi zabwino zambiri chifukwa cha mawu ake
ndipo ntchito zimene munthu agwira ndi manja ake zimamupindulira.

15 Zochita za chitsiru mwini wakeyo amaziona ngati zabwino,
koma munthu wanzeru amamvera malangizo.

16 Mkwiyo wa chitsiru umadziwika nthawi yomweyo,
koma munthu wanzeru sasamala kunyozedwa.

17 Woyankhula zoona amapereka umboni woona,
koma mboni yabodza imafotokoza zonama.

18 Munthu woyankhula mosasamala mawu ake amalasa ngati lupanga,
koma mawu a munthu wanzeru amachiritsa.

19 Mawu woona amakhala mpaka muyaya
koma mawu abodza sakhalitsa.

20 M'mitima ya anthu amene amakonza zoyipa muli chinyengo;
koma anthu olimbikitsa za mtendere amakhala ndi chimwemwe.

21 Palibe choyipa chimene chimagwera munthu wolungama,
koma munthu woyipa mavuto samuthera.

22 Pakamwa pa bodza pamamunyansa Yehova,
koma amakondwera ndi anthu oyankhula zoona.

23 Munthu wochenjera amabisa nzeru zake,
koma munthu wopusa amaonetsa uchitsiru wake poyera.

24 Ogwira ntchito mwakhama adzalamulira,
koma aulesi adzakhala ngati kapolo.

25 Nkhawa imakhala ngati katundu wolemera mu mtima mwa munthu,
koma mawu abwino amamusangalatsa.

26 Munthu wolungama amatsogolera mnansi wake,
koma ntchito za anthu oyipa zimawasocheretsa.

27 Munthu waulesi sapeza chimene akufuna,
koma munthu wakhama amapeza chuma chamtengo wapatali.

28 M'njira yachilungamo muli moyo;
koma njira ya munthu woyipa imafikitsa ku imfa.

# 13

1 Mwana wanzeru amamvera malangizo a abambo ake,
koma mwana wonyoza samamvetsera chidzudzulo.

2 Munthu amapeza zinthu zabwino chifukwa cha mawu ake,
koma anthu osakhulupirika amalakalaka zachiwawa basi.

3 Iye amene amagwira pakamwa pake amateteza moyo wake,
koma amene amayankhula zopanda pake adzawonongeka.

4 Munthu waulesi amakhumbira zinthu koma sapeza kanthu,
koma munthu wakhama adzalemera.

5 Munthu wolungama amadana ndi zabodza,
koma zochita za munthu woyipa zimanyansa ndiponso zimachititsa manyazi.

6 Chilungamo chimateteza munthu wangwiro,
koma tchimo limagwetsa munthu wochimwa.

7 Wina amadziyesa kuti ndi wolemera chonsecho alibe kanthu kalikonse;
munthu wina amaoneka ngati wosauka chonsecho ali ndi chuma chambiri.

8 Chuma cha munthu wolemera chitha kuwombola moyo wake,
koma munthu wosauka amamva chidzudzulo.

9 Nyale ya munthu wolungama ndi yokondweretsa,
koma nyale ya munthu woyipa imazimitsidwa.

10 Chipongwe chosamalabadirako za anthu ena chimadzetsa mikangano,
koma womva malangizo a anzawo ndiwo ali ndi nzeru.

11 Chuma chochipeza mofulumira chidzatha pang'onopang'ono
koma chuma chosonkhanitsidwa pang'onopang'ono chidzachulukirachulukira.

12 Chinthu chochiyembekezera chikalephereka chimalefula mtima,
koma chinthu chochilakalaka chikachitikadi chimakhala ngati mtengo wamoyo.

13 Amene amanyoza malangizo adzawonongeka,
koma amene amasamala lamulo amalandira mphotho.

14 Malangizo a munthu wanzeru ali ngati kasupe wamoyo;
amathandiza munthu kuti asakondwe mu msampha wa imfa.

15 Munthu wa nzeru zabwino amapeza kuyanja pakati pa anthu,
koma munthu wosakhulupirika adzawonongeka.

16 Munthu wochenjera amachita zinthu mwanzeru,
koma chitsiru chimaonetsa poyera uchitsiru wake.

17 Wamthenga woyipa amagwetsa anthu m'mavuto,
koma nthumwi yodalirika imabweretsa mtendere.

18 Wokana mwambo adzasauka ndi kunyozedwa,
koma wosamala chidzudzulo adzalemekezedwa.

19 Chinthu chochilakalaka chikachitika chimasangalatsa mtima,
koma zitsiru zimadana ndi kuleka zoyipa.

20 Woyenda ndi anthu anzeru nayenso adzakhala wanzeru;
koma woyenda ndi zitsiru adzapwetekeka.

21 Choyipa chitsata mwini,
koma wochita zolungama adzalandira mphotho yabwino.

22 Munthu wabwino amasiyira zidzukulu zake cholowa,
koma chuma cha munthu wochimwa amachilandira ndi olungama.

23 Tsala la munthu wosauka limalola chakudya chambiri,
koma anthu opanda chilungamo amachilanda.

24 Amene sakwapula mwana wake, ndiye kuti amamuda,
koma wokonda mwana wake sazengereza kumulanga.

25 Munthu wolungama amakhala ndi zakudya zoti adye n'kukhuta,
koma m'mimba mwa munthu woyipa mumakhala pululu ndi njala.

# 14

1 Mkazi wanzeru amamanga banja lake,
koma mkazi wopusa amalimasula ndi manja ake omwe.

2 Amene amayenda molungama amaopa Yehova,
koma amene njira zake ndi zoyipa amanyoza Yehova.

3 Kuyankhula kwa chitsiru kumamuyitanira ndodo pa msana,
koma milomo ya munthu wanzeru imamuteteza.

4 Pakasowa ng'ombe zolima gome limakhala lopanda chakudya,
koma pakakhala ng'ombe zamphamvu zakudya zimachulukanso.

5 Mboni yokhulupirika sinama,
koma mboni yonyenga imayankhula zabodza.

6 Wonyoza anzake amafunafuna nzeru koma osayipeza,
koma munthu womvetsa bwino amadziwa zinthu msanga.

7 Khala kutali ndi munthu wopusa
chifukwa sudzapeza mawu a nzeru.

8 Nzeru za munthu wochenjera zagona pakuzindikira njira zake.
Koma uchitsiru wa zitsiru umapusitsidwa ndi chinyengo chawo chomwe.

9 Zitsiru zimanyoza za kulapa machimo, awo,
koma kufuna kwabwino kumapezeka mwa anthu olungama.

10 Mtima uliwonse umadziwa wokha zowawa zake,
ndipo palibe wina aliyense angadziwe kukondwa kwake.

11 Nyumba ya munthu woyipa idzapasuka,
koma tenti ya munthu wowongoka mtima idzakhazikika.

12 Pali njira ina yooneka ngati yabwino kwa munthu,
koma kumatsiriziro kwake ndi ku imfa.

13 Ngakhale poseka mtima utha kumva kuwawa,
ndipo mathero achimwemwe akhoza kukhala chisoni.

14 Munthu wosakhulupirika adzalandira zogwirizana ndi ntchito yake,
koma munthu wabwino adzalandira mphotho ya ntchito yake.

15 Munthu wopusa amakhulupirira chilichonse,
koma munthu wochenjera amaganizira bwino mayendedwe ake.

16 Munthu wanzeru amaopa Mulungu ndipo amapewa zoyipa,
koma munthu wopusa ndi wokula mtima amakhala wosasamala.

17 Munthu wopsa mtima msanga amachita zinthu za uchitsiru,
ndipo anthu amadana ndi munthu wachinyengo.

18 Anthu opusa amalandira uchitsiru,
koma anthu ochenjera amavekedwa chipewa cha ulemerero wa kudziwa zinthu.

19 Anthu oyipa adzagwada pamaso pa anthu abwino,
ndipo anthu oyipa adzapempha thandizo kwa anthu olungama.

20 Munthu wosauka ngakhale anansi ake omwe amamuda,
koma munthu wolemera ali ndi abwenzi ambiri.

21 Wonyoza mnansi wake ndi wochimwa
koma ndi wodala amene amachitira chifundo anthu osowa.

22 Kodi amene amakonzekera zoyipa sasochera?
Koma amene amakonzekera zabwino anthu amawaonetsa chikondi ndi kukhulupirika.

23 Ntchito iliyonse imakhala ndi phindu,
koma kuyankhulayankhula kumabweretsa umphawi.

24 Chipewa chaulemu cha anthu a nzeru ndi chuma chawo chomwe,
koma malipiro a zitsiru ndi uchitsiru.

25 Mboni yokhulupirika imapulumutsa miyoyo,
koma mboni yabodza imaphetsa.

26 Amene amaopa Yehova ali ndi chitetezo chokwanira
ndipo iye adzakhala pothawira pa ana ake.

27 Kuopa Yehova ndiye kasupe wamoyo,
kumathandiza munthu kuti apewe msampha wa imfa.

28 Gulu lalikulu la anthu ndiye ulemerero wa mfumu,
koma popanda anthu kalonga amawonongeka.

29 Munthu wosapsa mtima msanga amamvetsa zinthu kwambiri,
koma munthu wopsa mtima msanga amaonetsa uchitsiru wake.

30 Mtima wodekha umapatsa thupi moyo,
koma nsanje imawoletsa mafupa.

31 Amene amapondereza m’mphawi amanyoza mlengi wake,
koma wochitira chifundo munthu wosowa amalemekeza Mulungu.

32 Anthu oyipa adzakanthidwa chifukwa cha ntchito zawo zomwe,
koma olungama adzatetezedwa mwa imfa yawo.

33 Nzeru zimakhala mu mtima mwa anthu omvetsa zinthu,
koma nzeru sipezeka mu mtima mwa zitsiru.

34 Chilungamo chimakweza mtundu wa anthu,
koma uchimo umachititsa manyazi mtundu uliwonse.

35 Mfumu imasangalatsidwa ndi wantchito wanzeru,
koma imachitira ukali wantchito wochititsa manyazi.

# 15

1 Kuyankha kofatsa kumathetsa mkwiyo,
koma mawu ozaza amautsa ukali.

2 Munthu wanzeru amayankhula zinthu za nzeru,
koma pakamwa pa zitsiru pamatulutsa za uchitsiru.

3 Maso a Yehova ali ponseponse,
amayang’ana pa oyipa ndi abwino omwe.

4 Kuyankhula kodekha kuli ngati mtengo wopatsa moyo,
koma kuyankhula kopotoka kumapweteka mtima.

5 Chitsiru chimanyoza mwambo wa abambo ake,
koma wochenjera amasamala chidzudzulo.

6 Munthu wolungama amakhala ndi chuma chambiri,
zimene woyipa amapindula nazo zimamugwetsa m’mavuto.

7 Pakamwa pa anthu anzeru pamafalitsa nzeru;
koma mitima ya zitsiru sitero.

8 Nsembe za anthu oyipa zimamunyansa Yehova,
koma amakondwera ndi pemphero la anthu owona mtima.

9 Ntchito za anthu oyipa zimamunyansa Yehova
koma amakonda amene amafunafuna chilungamo.

10 Amene amasiya njira yabwino adzalangidwa koopsa.
Odana ndi chidzudzulo adzafa.

11 Manda ndi chiwonongeko ndi zosabisika pamaso pa Yehova,
nanji mitima ya anthu!

12 Wonyoza sakonda kudzudzulidwa;
iye sapita kwa anthu anzeru.

13 Mtima wokondwa umachititsa nkhope kukhala yachimwemwe,
koma mtima wosweka umawawitsa moyo.

14 Mtima wa munthu wozindikira zinthu umafunafuna nzeru,
koma pakamwa pa zitsiru pamadya uchitsiru wawo.

15 Munthu woponderezedwa masiku ake onse amakhala oyipa,
koma mtima wachimwemwe umakhala pa chisangalalo nthawi zonse.

16 Kuli bwino kukhala ndi zinthu pang'ono n'kumaopa Yehova,
kusiyana ndi kukhala ndi chuma chambiri uli pamavuto.

17 Kuli bwino kudyera ndiwo zamasamba pamene pali chikondi,
kusiyana ndi kudyera nyama yang'ombe yonenepa pamene pali udani.

18 Munthu wopsa mtima msanga amayambitsa mikangano,
koma munthu woleza mtima amathetsa ndewu.

19 Njira ya munthu waulesi ndi yowirira ndi mtengo waminga,
koma njira ya munthu wolungama ili ngati msewu waukulu.

20 Mwana wanzeru amakondweretsa abambo ake,
koma mwana wopusa amanyoza amayi ake.

21 Uchitsiru umakondweretsa munthu wopanda nzeru,
koma munthu womvetsa zinthu amayenda mowongoka.

22 Popanda uphungu zolinga zako munthu zimalephereka,
koma pakakhala aphungu ambiri zolinga zimatheka.

23 Munthu amakondwera ndi kuyankha koyenera,
ndipo mawu onena pa nthawi yake ndi okoma.

24 Munthu wanzeru amatsata njira yopita ku moyo
kuti apewe malo okhala anthu akufa.

25 Yehova amapasula nyumba ya munthu wonyada
koma amasamalira malo a mkazi wamasiye.

26 Maganizo a anthu oyipa amamunyansa Yehova,
koma mawu a anthu oyera mtima amamusangalatsa.

27 Munthu wofuna phindu mwachinyengo amavutitsa banja lake,
koma wodana ndi ziphuphu adzakhala ndi moyo.

28 Munthu wolungama amaganizira za mmene ayankhire,
koma pakamwa pa munthu woyipa pamatulutsa mawu oyipa.

29 Yehova amakhala kutali ndi anthu oyipa,
koma amamva pemphero la anthu olungama.

30 Kuwala kwa maso kumasangalatsa mtima
ndipo uthenga wabwino umalimbitsa munthu.

31 Womvera mawu a chidzudzulo amene apatsa moyo
adzakhala pakati pa anthu anzeru.

32 Amene amanyoza mwambo amadzinyoza yekha,
koma womvera mawu a chidzudzulo amapeza nzeru zomvetsa zinthu.

33 Kuopa Yehova kumaphunzitsa munthu nzeru,
ndipo kudzichepetsa ndi ulemu chili patsogolo ndi kudzichepetsa.

# 16

1 Zolinga za mu mtima ndi za munthu,
koma kwa Yehova ndiye kumachokera yankho.

2 Zochita zonse za munthu zimaoneka zabwino pamaso pake,
koma Yehova ndiye amasanthula zolinga zako.

3 Pereka ntchito zako zonse m'manja mwa Yehova,
ndipo zolinga zako zidzachitikadi.

4 Yehova amachita zonse ndi cholinga chake,
ngakhale anthu oyipa kuti aone tsiku latsoka.

5 Munthu aliyense wodzikuza amamunyansa Yehova.
Koma dziwani izi: Iwo sadzakhala osalangidwa.

6 Chifukwa cha chikondi chosasinthika ndi kukhulupirika, munthu amakhululukidwa machimo ake;
chifukwa cha kuopa Yehova munthu amapewa zoyipa.

7 Pamene makhalidwe a munthu akondweretsa Yehova,
ngakhale adani ake amakhala naye mwa mtendere.

8 Kuli bwino kukhala ndi zinthu pang'ono zozipeza mwachilungamo,
kusiyana ndi kukhala ndi zinthu zambiri zozipeza popanda chilungamo.

9 Mtima wa munthu umalingalira zochita,

koma Yehova ndiye amakhazikitsa njira zake.

10 Mawu a mfumu ali ngati mawu ochokera kwa Mulungu;
ndipo pakamwa pake sipalakwa poweruza mlandu.

11 Miyeso ndi masikelo achilungamo zimachokera kwa Yehova;
miyala yonse yoyesera ya m'thumba anayipanga ndi Yehova.

12 Kuchita zoyipa kumanyansa mafumu,
pakuti chilungamo ndiye maziko a ufumu wake.

13 Mawu owona amakondweretsa mfumu.
Iyo imakonda munthu woyankhula choonadi.

14 Ukali wa mfumu ndi mthenga wa imfa,
koma munthu wanzeru amawupepesa ukaliwo.

15 Kuwala kwa nkhope ya mfumu kumapatsa moyo;
ndipo kukoma mtima kwake kuli ngati mitambo ya mvula nthawi ya chilimwe.

16 N'kwabwino kwambiri kupeza nzeru kupambana golide.
Kukhala womvetsa bwino zinthu n'kwabwino kupambana ndi kukhala ndi siliva.

17 Msewu wa munthu wowongoka mtima umapewa zoyipa;
wopenyetsetsa kumene akupita amasunga moyo wake.

18 Kunyada kumafikitsa ku chiwonongeko,
ndipo munthu wodzikuza adzagwa.

19 N'kwabwino kukhala ndi mtima wodzichepetsa pakati pa anthu oponderezedwa,
kusiyana ndi kugawana zolanda ndi anthu onyada.

20 Munthu womvera malangizo zinthu zimamuyendera bwino,
ndipo wodala ndi amene amadalira Yehova.

21 A mtima wanzeru amatchedwa ozindikira zinthu,
ndipo mawu ake okoma amawonjezera nzeru.

22 Kumvetsa zinthu ndi kasupe wa moyo kwa iwo amene ali nako,
koma uchitsiru umabweretsa chilango kwa zitsiru.

23 Mtima wanzeru umathandiza munthu kuyankhula mwa nzeru,
ndipo mawu ake amawonjezera nzeru.

24 Mawu okometsera ali ngati chisa cha njuchi,
amakoma mu mtima ndipo amalimbitsa thupi.

25 Pali njira ina yooneka ngati yowongoka kwa munthu
koma kumatsiriziro kwake ndi imfa.

26 Njala ya munthu wantchito imamuthandiza kulimbikira;
njalayo imamukakamiza kuchitapo kanthu.

27 Munthu wopanda pake amakonzekera kuchita zoyipa
ndipo mawu ake ali ngati moto wopsereza.

28 Munthu woyipa mtima amayambitsa mikangano,
ndipo miseche imalekanitsa anthu okondana kwambiri.

29 Munthu wandewu amakopa mnansi wake,
ndipo amamuyendetsa njira imene si yabwino.

30 Amene amatsinzinira maso ake amalingalira zinthu zokhota;
amene amachita msunamo amakonzeka kuchita zoyipa.

31 Imvi zili ngati chipewa chaufumu chaulemerero;
munthu amazipeza akakhala moyo wolungama.

32 Munthu wosapsa mtima msanga amaposa munthu wankhondo,
munthu wowugwira mtima wake amaposa amene amalanda mzinda.

33 Maere amaponyedwa pa mfunga,
koma ndiye Yehova amene amalongosola zonse.

## 17

1 N'kwabwino kudya mkute koma pali mtendere,
kuposa kuchita madyerero m'nyumba m'mene muli mikangano.

2 Kapolo wanzeru adzalamulira mwana wochititsa manyazi,
ndipo kapoloyo adzagawana nawo cholowa ngati mmodzi mwa abale.

3 Siliva amamuyesa m'ng'anjo ndipo golide amamuyesa m'ng'anjo,
koma Yehova amayesa mitima.

4 Munthu woyipa amamvera malangizo oyipa;
munthu wabodza amatchera khutu mawu osakaza.

5 Iye amene amalalatira m'mphawi amanyoza mlengi wake;
amene amakondwerera tsoka la mnzake sadzakhala osalangidwa.

6 Zidzukulu ndiye ulemu wa anthu okalamba,
ndipo makolo ndiye ulemerero wa ana.

7 Kuyankhula bwino sikuyenerana ndi chitsiru,
nanji kuyankhula bodza kungayenerane kodi ndi mfumu?

8 Chiphuphu chili ngati mankhwala amwayi kwa wochiperekayo;
kulikonse kumene amapita zinthu zimamuyendera.

9 Iye amene amakhululukira zolakwa za wina, amafunitsitsa chikondi;
wobwerezabwereza nkhani amapha chibwenzi.

10 Munthu wanzeru amamva kamodzi kokha,
munthu wopanda nzeru ndi samvamkunkhu.

11 Munthu woyipa maganizo ake ali pa kuwukira basi;
ndipo bwana adzamutumizira wamthenga wankhanza.

12 N'kwabwino kukumana ndi chimbalangondo cholandidwa ana ake
kusiyana ndi kukumana ndi chitsiru mu uchitsiru wake.

13 Ngati munthu abwezera choyipa kusinthana ndi zabwino,
ndiye choyipa sichidzachoka m'nyumba mwake.

14 Chiyambi cha mikangano chili ngati kukhamulira madzi,
choncho uzichokapo mkangano usanayambe.

15 Kumasula munthu wolakwa kapena kumanga munthu wosalakwa,
zonse ziwirizi Yehova zimamunyansa.

16 Ndalama zogulira nzeru zili ndi phindu lanji m'manja mwa chitsiru
poti iyeyo mutu wake sumayenda bwino?

17 Bwenzi lako limakukonda nthawi zonse,
ndipo m'bale wako anabadwa kuti azikuthandiza pamavuto.

18 Munthu wopanda nzeru amavomereza zopereka chikole
ndipo iyeyo amasanduka chikole cha mnansi wake.

19 Wokonda zolakwa amakonda mkangano,
ndipo wokonda kuyankhula zonyada amadziyitanira chiwonongeko.

20 Munthu wamtima woyipa zinthu sizimuyendera bwino;
ndipo woyankhula zachinyengo amagwa m'mavuto.

21 Mwana wopusa amamvetsa chisoni abambo ake,
abambo a chitsiru sakhala ndi chimwemwe.

22 Mtima wosangalala uli ngati mankhwala abwino,
koma mtima wokhumudwa umafowoketsa mafupa.

23 Munthu woyipa amalandira chiphuphu chamseri
kuti apotoze chiweruzo cholungama.

24 Munthu wozindikira zinthu, maso ake amakhala pa nzeru,
koma chitsiru chimwazamwaza maso ake pa dziko lonse lapansi.

25 Mwana wopusa amamvetsa chisoni abambo ake
ndipo amapweteketsa mtima amayi ake.

26 Sibwino kulipitsa munthu wosalakwa,
kapena kulanga anthu osalakwa.

27 Munthu wosunga pakamwa ndiye wodziwa zinthu,

ndipo wodekha mtima ndiye womvetsa bwino zinthu.

28 Ngakhale chitsiru chimakhala ngati chanzeru chikakhala chete;
ndipo chikatseka pakamwa chimakhala ngati munthu wochenjera.

# 18

1 Munthu wokonda kukhala yekha amafunafuna zomukomera yekha;
iye amatsutsana ndi malangizo onse anzeru.

2 Chitsiru chilibe chidwi chomvetsa zinthu,
koma chimakondwera ndi kuyankhula maganizo ake okha.

3 Kuyipa mtima kukabwera, manyozonso amabwera.
Manyazi amabwera pamodzi ndi kunyozeka.

4 Mawu a munthu ali ngati madzi akuya,
kasupe wa nzeru ndiye mtsinje wotumphuka.

5 Si kwabwino kukondera munthu woyipa pa milandu;
kapena kupondereza munthu wosalakwa.

6 Mawu a chitsiru amautsa mkangano;
pakamwa pake pamayitana mkwapulo.

7 Pakamwa pa chitsiru ndipo pamabweretsa chiwonongeko chake,
ndipo milomo yake ili ngati msampha wa moyo wake.

8 Mawu a miseche ali ngati chakudya chokoma;
amalowa m'mimba mwa munthu.

9 Munthu waulesi pa ntchito yake
ali pachibale ndi munthu amene amawononga zinthu.

10 Dzina la Yehova lili ngati nsanja yolimba;
wolungama amathawiramo napulumuka.

11 Chuma cha anthu olemera chili ngati mzinda wake wolimba;
chili ngati khoma lalitali limene amaganiza kuti limutchinjiriza.

12 Chiwonongeko chisanafike, mtima wa munthu umakhala wonyada,
koma ulemu umatsatira kudzichepetsa.

13 Ukayankha usanamvetse bwino nkhani,
umenewo ndi uchitsiru ndipo umachita manyazi.

14 Mtima wa munthu utha kupirira pa matenda,
koma munthu akataya mtima ndani angathe kumulimbitsanso.

15 Munthu wanzeru amawonjezera nzeru zina;
amafunafuna kudziwa bwino zinthu.

16 Mphatso ya munthu imamutsekulira njira

yomufikitsa pamaso pa anthu akuluakulu.

17 Amene amayamba kufotokoza mlandu wake amaoneka ngati wolungama ndiye
mpaka mnzake atabwera ndi kumufunsa bwino.

18 Kuchita maere kumathetsa mikangano;
amalekanitsa okangana amphamvu.

19 M'bale amene wamuthandiza amakhala ngati mzinda wolimba,
koma kukangana naye kumatsekereza thandizo.

20 Munthu amapeza bwino malingana ndi zoyankhula zake.
Adzakhuta ndi zipatso za pakamwa pake.

21 Mawu ako angathe kukuphetsa kapena kukukhalitsa moyo.
Wokonda kuyankhulayankhula adzadya zipatso zake.

22 Wapeza mkazi wapeza chinthu chabwino
ndipo Yehova amamukomera mtima.

23 Munthu wosauka amapempha
koma munthu wolemera amayankha mwaukali.

24 Pali abwenzi amene chibwenzi chawo n'chapamaso,
koma pali bwenzi limene limakukangamira kuposa m'bale wako.

## 19

1 Ndi wabwino munthu wosauka amene amayenda mu ungwiro,
aposa munthu wopusa woyankhula zokhota.

2 Si bwino kuti munthu akhale wopanda nzeru;
ndipo munthu woyenda mofulumira amaphonya njira.

3 Uchitsiru wa munthu umamubweretsera zovuta,
mtima wake umakwiyira Yehova.

4 Chuma chimachulukitsa abwenzi;
koma munthu wosauka bwenzi lake limamuthawa.

5 Mboni yonama sidzalephera kulangidwa;
ndipo iye amene amanena mabodza sadzapulumuka.

6 Anthu ambiri amafuna munthu wopatsa kuti awakomere mtima,
ndipo munthu amene amapereka mphatso ndi bwenzi la munthu aliyense.

7 Ngati munthu wosauka abale ake omwe amadana naye,
nanji abwenzi ake tsono!
Iwo adzamuthawa kupita kutali.
Amayesa kuwatsatira mowapembedza koma iwo samapezeka konse.

8 Iye amene amapeza nzeru ndiye kuti amakonda moyo wake.
Wosamalitsa kukhala wanzeru, zinthu zimamuyendera bwino.

9 Mboni yonama sidzalephera kulangidwa,
ndipo iye amene amanena mabodza adzawonongeka.

10 N'kosayenera kuti chitsiru chizikhala ndi moyo wamanyado,
nanjinso kuti kapolo azilamulira akalonga!

11 Nzeru zimapangitsa munthu kukhala wosakwiya msanga;
ulemerero wake uli posalabadira kuchitiridwa zoyipa.

12 Mkwiyo wa mfumu uli ngati kubangula kwa mkango,
koma kukoma mtima kwake kuli ngati mame pa udzu.

13 Mwana wopusa ndiye tsoka la abambo ake
ndipo mkazi wolongolola ndi wotopetsa ngati mvula yamvumbi.

14 Nyumba ndi chuma ndiye cholowa chochokera kwa makolo;
koma mkazi wanzeru ndi wochokera kwa Yehova.

15 Ulesi umagonetsa tulo tofa nato
ndipo munthu wosatakataka amakhala ndi njala.

16 Amene amamvera malangizo amasunga moyo wake,
koma amene sasamala malamulo a Yehova adzafa.

17 Amene amakomera mtima osauka amachita ngati wakongoletsa Yehova,
ndipo Yehovayo ndiye adzamubwezere.

18 Langa mwana wako, chiyembekezo chikanalipo;
ngati sutero udzawononga moyo wake.

19 Munthu waukali woopsa ayenera kulandira chilango;
pakuti akamulekelera ndiye zidzayipa kuposa kale.

20 Mvera uphungu ndipo landira malangizo;
pa mapeto pake udzakhala wanzeru.

21 Munthu amakonzekera zambiri mu mtima mwake,
koma cholinga cha Yehova ndiye chidzachitike.

22 Chimene munthu amafuna ndi chikondi chosatha;
n'kwabwino kukhala wosauka kusiyana ndi kukhala wabodza.

23 Kuopa Yehova kumabweretsa moyo;
wotereyo amakhala mu mtendere; ndiye kuti choyipa sichidzamugwera.

24 Munthu waulesi amapisa dzanja lake m'mbale;
koma sangathe kufikitsa dzanja lakelo pakamwa pake.

25 Menya munthu wonyoza, ndipo anthu opanda nzeru adzachenjererapo;
dzudzula munthu wozindikira zinthu, ndipo iye adzapezapo chidziwitso.

26 Mwana wochita ndewu ndi abambo ake ndi kuthamangitsa amayi ake,
ndi mwana wochititsa manyazi ndi wonyozetsa.

27 Mwana wanga, ukaleka kumvera malangizo,
udzapatukana ndi mawu opatsa nzeru.

28 Mboni yopanda pake imanyoza cholungama,
ndipo pakamwa pa anthu oyipa pamameza zoyipa.

29 Chilango chakonzedwa kale kuti chigwere anthu oyipa,
ndipo mkwapulo wakonzedwa kale kuti ukwapule misana ya anthu opusa.

## 20

1 Vinyo amachititsa munthu kukhala wonyoza ndipo chakumwa choledzeretsa chimachititsa munthu kukhala wolongolola;
aliyense wosochera nazo zimenezi alibe nzeru.

2 Ukali wa mfumu uli ngati kubangula kwa mkango;
amene amawuputa mkwiyowo amataya moyo wake.

3 N'chaulemu kwa munthu kupewa mikangano,
koma chitsiru chilichonse chimafulumira kulongolola.

4 Munthu waulesi satipula m'munda pa nthawi yoyenera;
kotero pa nthawi yokolola adzafunafuna zinthu koma sadzapeza kanthu kalikonse.

5 Zolinga za mtima wa munthu zili ngati madzi akuya,
munthu womvetsa zinthu ndiye yekha angawatunge.

6 Anthu ambiri amayankhula za kukhulupirika kwawo,
koma munthu wokhulupirika angamupeze ndani?

7 Munthu wolungama amakhala ndi makhalidwe abwino;
odala ndi ana ake amene amatsanzira moyo wake.

8 Mfumu ikhala pa mpando wake wa chiweruzo,
imapeta ndi maso ake anthu onse oyipa.

9 Ndani amene anganene kuti, "Ndawuyeretsa mtima wanga;
ndilibe tchimo lililonse?"

10 Masikelo ndi miyeso ya zinthu imene ili yachinyengo
zonsezi Yehova zimamunyansa.

11 Ngakhale mwana amadziwika ndi zochita zake,
ngati zochita zake zili zoyera ndi zoyenera.

12 Makutu amene amamva ndi maso amene amaona,
zonsezi anazilenga ndi Yehova.

13 Usakonde tulo ungasauke;
khala maso ndipo udzakhala ndi chakudya chambiri.

14 Munthu wogula chinthu amati, “Sichabwino, sichabwino.”
Koma akagula n’kuchokapo amayamba kudzitama.

15 Pali golide ndi miyala yamtengowapatali,
koma milomo yoyankhula zanzeru ndi yamtengowapatali koposa zonsezi.

16 Utenge chovala cha munthu amene waperekera mlendo chikole;
kuti chikhale chikole chako chifukwa waperekera chikole munthu wachilendo.

17 Chakudya chochipeza mwachinyengo chimukomera munthu,
koma pa mapeto pake chimasanduka ngati mchenga m’kamwa mwake.

18 Zokonzekera zimapindula utafunsira uphungu;
ndipo usanamenye nkhondo yamba wapempha malangizo oyenera.

19 Amene amanka nanena miseche amawulula zachinsinsi.
Choncho usamagwirizane naye munthu woyankhula zopusayo.

20 Ngati munthu atemberera abambo ake kapena amayi ake,
moyo wake udzazimitsidwa ngati nyale mu mdima wandiweyani.

21 Cholowa chochipeza mofulumira poyamba,
sichidzakhala dalitso pa mapeto pake.

22 Usanene kuti, “Ine ndidzabwezera choyipa chimenechi!”
Dikira Yehova, ndipo Iye adzakupulumutsa.

23 Miyeso yosintha imamunyansa Yehova;
ndipo masikelo onyenga si abwino.

24 Mayendedwe a munthu amawalamulira ndi Yehova,
tsono munthu angadziwe bwanji njira yake?

25 Ndi msampha kwa munthu kuyankhula mofulumira kuti “Chinthu ichi n’chopatulika kwa Yehova,”
popeza mwina atha kusintha maganizo utalumbira kale.

26 Mfumu ya nzeru imapeta kwathunthu
anthu oyipa.

27 Mpweya wa munthu uli ngati nyale ya Yehova;
imafufuza ziwalo zake zonse zam’kati.

28 Kukoma mtima ndi kukhulupirika ndizo zimasunga mfumu;
chilungamo chimalimbikitsa mpando wake waufumu.

29 Ulemerero wa achinyamata uli mu mphamvu zawo,
imvi ndi ulemerero wa anthu okalamba.

30 Mikwingwirima yopweteka ndiyo imachotsa zoyipa,
ndipo mikwapulo ndiyo imachotsa zam'katikati mwa munthu.

# 21

1 Mtima wa mfumu uli ngati mtsinje wamadzi m'dzanja la Yehova;
Iye amautsongolera pa chilichonse chimene akufuna.

2 Makhalidwe a munthu amaoneka olungama kwa mwini wakeyo,
koma Yehova ndiye amayesa mtima wake.

3 Za chilungamo ndi zolondola
ndi zomwe zimakondweretsa Yehova kuposa kupereka nsembe.

4 Maso odzikuza ndi mtima wonyada,
zimatsogolera anthu oyipa ngati nyale n'chifukwa chake amachimwa.

5 Zolinga za munthu wakhama zimachulukitsa zinthu zake;
koma aliyense wochita zinthu mofulumira amadzakhala wosauka.

6 Chuma chochipeza ndi mawu onyenga ndi chosakhalitsa
ndipo chimakola anthu mu msampha wa imfa.

7 Chiwawa cha anthu oyipa chidzawawononga,
pakuti iwo amakana kuchita zolungama.

8 Njira ya munthu wolakwa ndi yokhotakhota,
koma makhalidwe a munthu wosalakwa ndi olungama.

9 N'kwabwino kukhala wekha pa ngodya ya denga la nyumba,
kuposa kukhala m'nyumba pamodzi ndi mkazi wolongolola.

10 Munthu woyipa amalakalaka zoyipa;
sachitira chifundo mnansi wake wovutika.

11 Munthu wonyoza akalangidwa, anthu opusa amapeza nzeru;
koma munthu wanzeru akalangizidwa, amapeza chidziwitso.

12 Zolingalira za munthu woyipa n'zosabisika pamaso pa Yehova,
ndipo Iye adzawononga woyipayo.

13 Amene atsekera m'khutu mwake wosauka akamalira,
nayenso adzalira koma palibe adzamuyankhe.

14 Mphatso yoperekedwa mseri imathetsa mkwiyo,

ndipo chiphuphu choperekedwa mobisa chimathetsa mphamvu ya
ukali woopsa.

15 Chilungamo chikachitika anthu olungama amasangalala,
koma anthu oyipa amaopsedwa nazo.

16 Munthu amene amachoka pa njira ya anthu anzeru
adzapezeka m'gulu la anthu akufa.

17 Aliyense wokonda zisangalalo adzasanduka m'mphawi,
ndipo wokonda vinyo ndi mafuta sadzalemera.

18 Anthu oyipa adzakhala chowombolera cha anthu olungama
ndipo osakhulupirika chowombolera anthu olungama mtima.

19 N'kwabwino kukhala m'chipululu
kuposa kukhala ndi mkazi wolongolola ndi wopsa mtima msanga.

20 Munthu wanzeru samwaza chuma chake,
koma wopusa amachiwononga.

21 Amene amatsata chilungamo ndi kukhulupirika,
amapeza moyo ndi ulemerero.

22 Munthu wanzeru amagonjetsa mzinda wa anthu amphamvu
ndi kugwetsa linga limene iwo amalidalira.

23 Amene amagwira pakamwa pake ndi lilime lake
sapeza mavuto.

24 Munthu wonyada ndi wodzikuza amamutcha, "Mnyodoli,"
iye amachita zinthu modzitama kwambiri.

25 Chilakolako cha munthu waulesi chidzamupha yekha
chifukwa manja ake amangokhala goba osagwira ntchito.
26 Tsiku lonse anthu oyipa amasirira zambiri,
koma anthu olungama amapereka mowolowamanja.

27 Nsembe ya anthu oyipa imamunyansa Yehova,
nanji akayipereka ndi cholinga choyipa!

28 Mboni yonama idzawonongeka,
koma mawu a munthu wakumva adzakhala nthawi zonse.

29 Munthu woyipa amafuna kudzionetsa ngati wolimba mtima,
koma munthu wowongoka amaganizira njira zake.

30 Palibe nzeru, palibe kumvetsa bwino, palibenso uphungu,
zimene zingapambane Yehova.

31 Kavalo amamukonzera tsiku la nkhondo,

koma ndi Yehova amene amapambanitsa.

## 22

1 Mbiri yabwino ndi yofunika kuposa chuma chambiri;
kupeza kuyanja n'kwabwino kuposa siliva kapena golide.

2 Wolemera ndi wosauka ndi ofanana;
onsewa anawalenga ndi Yehova.

3 Munthu wochenjera akaona choopsa amabisala,
koma munthu wopusa amangopitirira ndipo amadzanong'oneza bondo.

4 Mphotho ya munthu wodzichepetsa
ndi woopa Yehova ndi chuma, ulemu ndi moyo.

5 M'njira za anthu oyipa muli minga ndi misampha,
koma amene amasala moyo wake adzazipewa zonsezo.

6 Mwana muzimuphunzitsa njira yake,
ndipo akadzakalamba sadzachokamo.

7 Wolemera amalamulira wosauka,
ndipo wokongola zinthu amakhala kapolo wa womukongozayo.

8 Amene amafesa zoyipa amakolola mavuto,
ndipo ndodo yaukali wake idzathyoka.

9 Amene ali ndi diso lachifundo adzadalitsika,
pakuti iye amagawana chakudya chake ndi anthu osauka.

10 Chotsani munthu wonyoza, ndipo kukangana kudzatha;
mapokoso ndi zonyoza zidzaleka.

11 Amene amakonda kukhala woyera mtima ndi kumayankhula mawu abwino,
adzakhala bwenzi la mfumu.

12 Maso a Yehova amakhala pa anthu odziwa bwino zinthu,
koma Iye adzalepheretsa mawu a anthu osakhulupirika.

13 Munthu waulesi amati,
"Kunjaku kuli mkango. Ine ndidzaphedwa m'misewu!"

14 Pakamwa pa mkazi wachigololo pali ngati dzenje lozama;
amene Yehova wamukwiyira adzagwamo.

15 Uchitsiru umakhala mu mtima mwa mwana,
koma ndodo yomulangira mwanayo idzachotsa uchitsiruwo.

16 Amene amapondereza anthu osauka kuti awonjezere chuma chake,

ndiponso amene amapereka mphatso kwa anthu olemera onsewa adzasauka.

*Malangizo a Anthu Anzeru*

17 Utchere khutu lako ndipo umvere mawu anzeru;
uyike mtima wako pa zimene ndikukuphunzitsa kuti udziwe.
18 Zidzakhala zokondweretsa ngati uzisunga mu mtima mwako
ndi wokonzeka kuziyankhula.
19 Ndakuphunzitsa zimenezi lero
koma makamaka uziopa Yehova.
20 Kodi suja ndinakulembera malangizo makumi atatu
okuchenjeza ndi okupatsa nzeru,
21 malangizo okudziwitsa zolungama
ndi zoona
ndi kuti ukawayankhe zoona amene akutumawo?

22 M'mphawi usamubere chifukwa ndi osauka,
ndipo usawapondereze anthu osowa m'bwalo la milandu,
23 pakuti Yehova adzawateteza pa mlandu wawo
ndipo adzalanda moyo onse amene amawalanda iwo.

24 Usapalane naye ubwenzi munthu wosachedwa kupsa mtima
ndipo usayanjane ndi munthu amene sachedwa kukwiya
25 kuopa kuti iwe ungadzaphunzire njira zake
ndi kukodwa mu msampha.

26 Usakhale munthu wopereka chikole
kapena kukhala mboni pa ngongole;
27 ngati ulephera kupeza njira yolipirira
adzakulanda ngakhale bedi lako lomwe.

28 Usasunthe mwala wam'malire akalekale
amene anayikidwa ndi makolo ako.

29 Kodi ukumuona munthu waluso pa ntchito yake?
Iye adzatumikira mafumu;
sadzatumikira anthu wamba.

# 23

1 Ngati ukhala pansi kuti udye pamodzi ndi wolamulira,
uyang'ane bwino zimene zili pamaso pako,
2 ngati ndiwe munthu wadyera
udziletse kuti usaonetse dyera lakolo.
3 Usasirire zakudya zake,
pakuti zimenezo ndi zakudya zachinyengo.

4 Usadzitopetse wekha ndi kufuna chuma,
ukhale ndi nzeru ya kudziretsa.
5 Ukangoti wachipeza chumacho uwona posachedwa kuti palibepo.
Chumacho chimachita ngati chamera mapiko mwadzidzidzi
ndi kuwuluka kunka kumwamba ngati chiwombankhanga.

6 Usadye chakudya cha munthu waumbombo,
usalakalake zakudya zake zokoma;
7 paja iye ndi munthu amene
nthawi zonse amaganizira za mtengo wake
ngakhale amati kwa iwe, “Idya ndi kumwa,”
koma sakondweretsedwa nawe.
8 Udzasanza zimene wadyazo
ndipo mawu ako woyamikira adzapita pachabe.

9 Usayankhule munthu wopusa akumva,
pakuti adzanyoza mawu ako anzeru.

10 Usasunthe mwala wa m’malire akalekale
kapena kulowerera m’minda ya ana amasiye,
11 paja Mpulumutsi wawo ndi wamphamvu;
iye adzawateteza pa milandu yawo kutsutsana nawe.

12 Mtima wako uzikhala pa malangizo
ndipo makutu ako azimvetsera mawu a chidziwitso.

13 Usaleke kumulangiza mwana;
ngati umulanga ndi chikwapu sadzafa.
14 Ukamukwapula ndi tsatsa
udzapulumutsa moyo wake.

15 Mwana wanga, ngati mtima wako ukhala wanzeru,
inenso mtima wanga udzakondwera.
16 Mtima wanga udzakondwera
pamene ndidzakumva ukuyankhula zolungama.

17 Mtima wako usachite nsanje ndi anthu ochimwa,
koma uziopa Yehova tsiku ndi tsiku.
18 Ndithu za m’tsogolo zilipo
ndipo chiyembekezo chakocho sichidzalephereka.

19 Tamvera mwana wanga, ndipo ukhale wanzeru,
mtima wako uwuyendetse m’njira yabwino.
20 Usakhale pakati pa anthu amene amaledzera
kapena pakati pa anthu amene amadya nyama mwadyera.
21 Paja anthu oledzera ndi adyera amadzakhala amphawi
ndipo aulesi adzavala sanza.

22 Mvera abambo ako amene anakubala,
usanyoze amayi ako pamene akalamba.
23 Gula choonadi ndipo usachigulitse;
ugulenso nzeru, mwambo ndiponso kumvetsa zinthu bwino.
24 Abambo a munthu wolungama ali ndi chimwemwe chachikulu;
Wobala mwana wanzeru adzakondwera naye.
25 Abambo ndi amayi ako asangalale;
amene anakubereka akondwere!

26 Mwana wanga, undikhulupirire

ndipo maso ako apenyetsetse njira zanga.
27 Paja mkazi wachiwerewere ali ngati dzenje lozama;
ndipo mkazi woyendayenda ali ngati chitsime chopapatiza.
28 Amabisala ngati mbala yachifwamba,
ndipo amuna amakhala osakhulupirika chifukwa cha iyeyu.

29 Ndani ali ndi tsoka? Ndani ali ndi chisoni?
Ndani ali pa mkangano? Ndani ali ndi madandawulo?
Ndani ali ndi zipsera zosadziwika uko zachokera? Ndani ali ndi maso ofiira?
30 Ndi amene amakhalitsa pa mowa,
amene amapita nalawa vinyo osakanizidwa.
31 Usatengeke mtima ndi kufiira kwa vinyo,
pamene akuwira m'chikho
pamene akumweka bwino!
32 Potsiriza pake amaluma ngati njoka,
ndipo amajompha ngati mphiri.
33 Maso ako adzaona zinthu zachilendo
ndipo maganizo ndi mawu ako adzakhala osokonekera.
34 Udzakhala ngati munthu amene ali gone pakati pa nyanja,
kapena ngati munthu wogona pa msonga ya mlongoti ya ngalawa.
35 Iwe udzanena kuti, "Anandimenya, koma sindinapwetekedwe!
Andimenya koma sindinamve kanthu!
Kodi ndidzuka nthawi yanji?
Ndiye ndifunefunenso vinyo wina."

# 24

1 Usachitire nsanje anthu oyipa,
usalakalake kuti uzikhala nawo,
2 pakuti mitima yawo imalingalira chiwawa,
ndipo pakamwa pawo pamayankhula zoyambitsa mavuto.

3 Nyumba imamangidwa ndi anthu anzeru,
ndipo imakhazikika ndi anthu odziwa zinthu;
4 Munthu wodziwa zinthu angathe kudzaza zipinda zake
ndi chuma chamtengowapatali ndiponso chabwino.

5 Munthu wodziwa zinthu ali ndi mphamvu yayikulu kuposa munthu wanyonga zambiri,
ndipo munthu wachidziwitso amaposa munthu wamphamvu.
6 Pafunika malangizo kuti ukamenye nkhondo.
Pakakhala aphungu ambiri kupambana kumakhalapo.

7 Nzeru ndi chinthu chapatali kwambiri kwa chitsiru;
chilibe choti chiyankhule pabwalo la milandu pa chipata.

8 Amene amakonzekera kuchita zoyipa
adzatchedwa mvundulamadzi.
9 Kukonzekera kuchita za uchitsiru ndi tchimo,
ndipo munthu wonyoza amanyansa anthu.

10 Ngati utaya mtima nthawi ya mavuto ndiye kuti

mphamvu yako ndi yochepadi!

11 Uwapulumutse amene akutengedwa kuti akaphedwe;
uwalanditse amene akuyenda movutika kupita kokaphedwa.
12 Ukanena kuti, “Koma ife sitinadziwe kanthu za izi,”
kodi Iye amene amasanthula mtima sazindikira zimenezi?
Kodi Iye amene amateteza moyo wako sazidziwa zimenezi?
Kodi Iye sadzalipira munthu malingana ndi ntchito zake?

13 Mwana wanga, uzidya uchi popeza ndi wabwino;
uchi wochokera m'chisa cha njuchi ndi wokoma ukawulawa.
14 Udziwe kuti nzeru ndi yoteronso pa moyo wako;
ngati uyipeza nzeruyo, zinthu zidzakuyendera bwino m'tsogolo,
ndipo chiyembekezo chako sichidzapita pachabe.

15 Usachite zachifwamba nyumba ya munthu wolungama ngati munthu woyipa.
Usachite nayo nkhondo nyumba yake;
16 paja munthu wolungama akagwa kasanu n'kawiri amadzukiriranso.
Koma woyipa adzathedwa tsoka likadzawafikira.

17 Usamakondwera ndi kugwa kwa mdani wako.
Mtima wako usamasangalale iye akapunthwa.
18 Kuopa kuti Yehova ataziona zimenezi nayipidwa nazo,
angaleke kukwiyira mdaniyo.

19 Usavutike mtima chifukwa cha anthu ochita zoyipa
kapena kuchitira nsanje anthu oyipa,
20 paja munthu woyipa alibe tsogolo.
Moyo wa anthu oyipa adzawuzimitsa ngati nyale.

21 Mwana wanga, uziopa Yehova ndi mfumu,
ndipo usamagwirizana ndi anthu owachitira mwano,
22 awiri amenewa amagwetsa tsoka mwadzidzidzi.
Ndani angadziwe mavuto amene angagwetse?

### *Malangizo Enanso a Anthu Anzeru*

23 Malangizo enanso a anthu anzeru ndi awa:
Kukondera poweruza mlandu si chinthu chabwino:
24 Aliyense amene amawuza munthu wolakwa kuti, “Iwe ndi munthu wosalakwa,”
anthu a mitundu yonse adzamutemberera, ndi mitundu ya anthu idzayipidwa naye.
25 Koma olanga anthu oyipa zinthu zidzawayendera bwino
ndipo madalitso ochuluka adzakhala pa iwo.

26 Woyankhula mawu owona
ndiye amaonetsa chibwenzi chenicheni.

27 Ugwiriretu ntchito zako zonse,
makamaka za ku munda
ndipo pambuyo pake uyambe kumanga nyumba.

28 Usakhale mboni yotsutsa mnzako popanda chifukwa,
kapena kugwiritsa ntchito pakamwa pako kunena zachinyengo.
29 Usanene kuti, “Ine ndidzamuchitira iye monga momwe wandichitira ine;
ndidzamubwezera munthu ameneyo zimene anandichitira.”

30 Ndinkayenda m’mbali mwa munda wa munthu waulesi
ndinadutsa munda wamphesa wa munthu wopanda nzeru.
31 Ndinapeza kuti paliponse m’mundamo munali mutamera minga,
m’nthaka imeneyo munali mutamera khwisa,
ndipo mpanda wake wamiyala unali utawonongeka.
32 Tsono nditaona ndinayamba kuganizira mu mtima mwanga
ndipo ndinatolapo phunziro ili:
33 Ukati, “Bwanji ndigone pang’ono,” kapena “Ndiwodzereko pang’ono,”
kapenanso “Ndipinde manja pang’ono kuti ndipumule,”
34 umphawi udzafika pa iwe ngati mbala
ndipo usiwa udzakupeza ngati munthu wachifwamba.

# 25

*Miyambo Ina ya Solomoni*

1 Iyi ndi miyambo inanso ya Solomoni, imene anthu a Hezekiya mfumu
ya ku Yuda analemba.
2 Ulemerero wa Mulungu uli pa kubisa zinthu;
ulemerero wa mafumu uli pa kufufuza zinthuzo.

3 Monga momwe kwatalikira kumwamba ndi momwe kulili kuzama kwa dziko lapansi,
ndi momwemonso alili maganizo a mfumu kusadziwika kwake.

4 Chotsa zoyipa m’siliva
ndipo wosula adzapanga naye ziwiya.
5 Chotsa munthu woyipa pamaso pa mfumu;
ndipo ufumu wake udzakhazikika mu chilungamo.

6 Usamadzikuze ukakhala pamaso pa mfumu,
ndipo usamakhale pamalo pa anthu apamwamba;
7 paja ndi bwino kuti mfumu ichite kukuwuza kuti, “Bwera pamwamba pano,”
kulekana ndi kuti ikuchititse manyazi chifukwa cha wina wokuposa.

Chimene wachiona ndi maso ako,
8 usafulumire kupita nacho ku bwalo la milandu
nanga udzachita chiyani pa mapeto pake
ngati mnansi wako adzakuchititsa manyazi?

9 Kamba mlandu ndi mnansi wako,
koma osawulula chinsinsi cha munthu wina
10 kuopa kuti wina akamva mawu ako adzakuchititsa manyazi
ndipo mbiri yako yoyipa sidzatha.

11 Mawu amodzi woyankhulidwa moyenera

ali ngati zokongoletsera zagolide m’zotengera zasiliva.

12 Kwa munthu womvetsa bwino, kudzudzula kwa munthu wanzeru kuli ngati ndolo zagolide
kapena chodzikongoletsera china cha golide wabwino kwambiri.

13 Wamthenga wodalirika ali ngati madzi ozizira pa nthawi yokolola
kwa anthu amene amutuma;
iye amaziziritsa mtima bwana wake.

14 Munthu wonyadira mphatso imene sayipereka
ali ngati mitambo ndi mphepo yopanda mvula.

15 Kupirira ndiye kumagonjetsa mfumu,
ndipo kufewa m’kamwa kutha kumafatsitsa munthu wowuma mtima.

16 Ngati upeza uchi, ingodya okukwanira,
kuopa ungakoledwe nawo ndi kuyamba kusanza.
17 Uzipita kamodzikamodzi ku nyumba ya mnzako
ukawirikiza kupita, udzadana naye.

18 Munthu wochitira mnzake umboni wonama,
ali ngati chibonga kapena lupanga kapena muvi wakuthwa.

19 Kudalira munthu wosankhulupirika pa nthawi ya mavuto,
kuli ngati dzino lobowoka kapena phazi lolumala.

20 Kuyimbira nyimbo munthu wachisoni
kuli ngati kuvula zovala pa nyengo yozizira
kapena kuthira mchere pa chilonda.

21 Ngati mdani wako ali ndi njala, mupatse chakudya kuti adye;
ngati ali ndi ludzu mupatse madzi kuti amwe.
22 Pochita izi, udzamusenzetsa makala a moto pa mutu pake,
ndipo Yehova adzakupatsa mphotho.

23 Monga momwe mphepo yampoto imabweretsera mvula,
chonchonso mjedu umadzetsa mkwiyo.

24 N’kwabwino kukhala pa ngodya ya denga
kuposa kukhala m’nyumba ndi mkazi wolongolola.

25 Mthenga wabwino wochokera ku dziko lakutali
ali ngati madzi ozizira kwa munthu waludzu.

26 Munthu wolungama amene amagonjera munthu woyipa
ali ngati kasupe wodzaza ndi matope kapena chitsime cha madzi oyipa.

27 Sibwino kudya uchi wambiri,
sibwinonso kudzifunira wekha ulemu.

28 Munthu amene samatha kudziretsa
ali ngati mzinda umene adani awuthyola ndi kuwusiya wopanda malinga.

## 26

1 Ngati chisanu choti mbee nthawi yachilimwe kapena mvula nthawi yokolola,
ndi momwe zilili ndi ulemu wowulandira chitsiru.

2 Ngati timba wokhalira kuwuluka kapena namzeze wokhalira kuzungulirazungulira,
ndi mmenenso limachitira temberero lopanda chifukwa, silichitika.

3 Mkwapulo ndi wokwapulira kavalo, chitsulo ndi cha m'kamwa mwa bulu,
choncho ndodo ndi yoyenera ku msana wa chitsiru.

4 Usayankhe chitsiru monga mwa uchitsiru wake,
kuopa kuti ungadzakhale ngati chitsirucho.

5 Koma nthawi zina umuyankhe monga mwa uchitsiru wake,
kuopa kuti angamadziyese yekha wanzeru.

6 Kutuma chitsiru kuti akapereke uthenga
kuli ngati kudzidula mapazi ndipo kumakuyitanira mavuto.

7 Monga miyendo ya munthu wolumala imene ilibe mphamvu
ndi mmene ulili mwambi m'kamwa mwa chitsiru.

8 Kupereka ulemu kwa chitsiru
zili ngati kukulunga mwala m'legeni.

9 Monga umachitira mtengo waminga wobaya m'dzanja la chidakwa
ndi mmene ulili mwambi m'kamwa mwa chitsiru.

10 Munthu amene amalemba ntchito chitsiru chongoyendayenda,
ali ngati woponya mivi amene angolasa anthu chilaselase.

11 Chitsiru chimene chimabwerezabwereza uchitsiru wake
chili ngati galu amene amabwerera ku masanzi ake.

12 Munthu wa uchitsiru aliko bwino popeza pali chiyembekezo
kuposana ndi munthu amene amadziyesa yekha kuti ndi wanzeru.

13 Munthu waulesi amati, “Mu msewu muli mkango,
mkango woopsa ukuyendayenda m'misewu!”

14 Monga chitseko chimapita uku ndi uku pa zolumikizira zake,
momwemonso munthu waulesi amangotembenukatembenuka pa bedi lake.

15 Munthu waulesi akapisa dzanja lake mu m'bale;

zimamutopetsa kuti alifikitse pakamwa pake.

16 Munthu waulesi amadziyesa yekha wanzeru
kuposa anthu asanu ndi awiri amene amayankha mochenjera.

17 Munthu wongolowera mikangano imene si yake
ali ngati munthu wogwira makutu a galu wongodziyendera.

18 Monga munthu wamisala amene
akuponya sakali zamoto kapena mivi yoopsa,
19 ndi momwe alili munthu wonamiza mnzake,
amene amati, "Ndimangoseka chabe!"

20 Pakasowa nkhuni, moto umazima;
chomwechonso pakasowa anthu amiseche mkangano umatha.

21 Monga alili makala pa moto wonyeka kapena mmene zimachitira nkhuni pa moto,
ndi mmene alili munthu wolongolola poyambitsa mikangano.

22 Mawu a munthu wamiseche ali ngati chakudya chokoma;
chimene chimatsikira m'mimba mwa munthu.

23 Monga mmene chiziro chimakutira chiwiya chadothi
ndi mmene mawu oshashalika amabisira mtima woyipa.

24 Munthu wachidani amayankhula zabwino
pamene mu mtima mwake muli chinyengo.
25 Ngakhale wotereyu mawu ake ali okoma, koma usamukhulupirire,
pakuti mu mtima mwake mwadzaza zonyansa.
26 Ngakhale amabisa chidani mochenjera,
koma kuyipa kwakeko kudzaonekera poyera pa gulu la anthu.

27 Ngati munthu akumba dzenje, adzagweramo yekha;
ngati munthu agubuduza mwala, udzamupsinja iye mwini.

28 Munthu wonama amadana ndi amene anawapweteka,
ndipo pakamwa poshashalika pamabweretsa chiwonongeko.

## 27

1 Usamanyadire za mawa,
pakuti sudziwa zimene zidzachitike pa tsikulo.

2 Munthu wina akutamande, koma osati wekha;
mlendo akakutamanda, ndiponi koma osati ndi pakamwa pako.

3 Mwala ndi wolemera ndipo mchenganso ndi wolemera kwambiri,
koma makani a chitsiru ndi oposa zonsezo kulemera kwake.

4 Mkwiyo umadzetsa nkhanza ndipo kupsa mtima kumachititsa zoopsa.
Koma nsanje imachita zoopsa zopambana.

5 Kudzudzula munthu poyera n'kwabwino
kuposa chikondi chobisika.

6 Munthu amene amakukonda ngakhale akupweteke zili bwino,
koma mdani wako amakupsompsona mwachinyengo.

7 Iye amene wakhuta amayipidwa ndi chisa cha uchi,
koma kwa munthu wanjala ngakhale chimene chili chowawa chimamukomera.

8 Munthu amene wasochera ku nyumba kwake,
ali monga mbalame imene yasochera pa chisa chake.

9 Mafuta ndi zonunkhira zimasangalatsa mtima,
ndipo kukoma mtima kwa bwenzi kwagona pa malangizo ake.

10 Usasiye bwenzi lako ndiponso bwenzi la abambo ako,
ndipo usapite ku nyumba ya m'bale wako pamene wakumana ndi mavuto;
mnzako wokhala naye pafupi amaposa m'bale wako wokhala kutali.

11 Mwana wanga, khala wanzeru, ndipo ukondweretse mtima wanga;
pamenepo ine ndidzatha kuyankha aliyense amene amandinyoza.

12 Munthu wochenjera akaona choopsa amabisala,
koma munthu wopusa amangopitirira ndipo amakumana ndi mavuto.

13 Utenge chovala cha munthu amene waperekera mlendo chikole;
ngati chigwiriro chifukwa waperekera chikole mlendo wosadziwika.

14 Ngati munthu apatsa mnzake moni mofuwula mmamawa kwambiri,
anthu adzamuyesa kuti akutemberera.

15 Mkazi wolongolola ali ngati
mvula yamvumbi.
16 Kumuletsa mkazi wotereyu zimenezi zili ngati kuletsa mphepo
kapena kufumbata mafuta m'dzanja.

17 Chitsulo chimanoledwa ndi chitsulo chinzake,
chomwechonso munthu amanoledwa ndi munthu mnzake.

18 Amene amasamalira mtengo wamkuyu adzadya zipatso zake,
ndipo iye amene amasamalira mbuye wake adzalandira ulemu.

19 Monga momwe nkhope imaonekera m'madzi,
chomwechonso mtima wa munthu umadziwika ndi ntchito zake.

20 Manda sakhuta,
nawonso maso a munthu sakhuta.

21 Siliva amasungunulira mu uvuni ndipo golide m'ng'anjo,

chomwechonso munthu amadziwika ndi zomwe akudzitamandira nazo.

22 Ngakhale utakonola chitsiru mu mtondo
ndi musi ngati chimanga,
uchitsiru wakewo sudzachoka.

23 Uzidziwe bwino nkhosa zako momwe zilili.
Kodi usamalire bwino ziweto zako?
24 Paja chuma sichikhala mpaka muyaya,
ndipo ufumu sukhala mpaka mibado yonse.
25 Pamene udzu watha, msipu n'kumera;
ndipo atatuta udzu wa ku mapiri,
26 ana ankhosa adzakupatsani chovala
ndipo pogulitsa mbuzi mudzapeza ndalama yogulira munda.
27 Mudzakhala ndi mkaka wambuzi wambiri
kuti muzidya inuyo ndi banja lanu
ndi kudyetsa antchito anu aakazi.

## 28

1 Munthu woyipa amathawa ngakhale palibe wina womuthamangitsa,
koma wolungama ndi wolimba mtima ngati mkango.

2 Pamene m'dziko muli kuwukirana, dzikolo limakhala ndi olamulira ambiri,
koma anthu omvetsa ndi odziwa zinthu bwino ndiwo angakhazikitse bata m'dzikolo nthawi yayitali.

3 Munthu wosauka amene amapondereza osauka anzake
ali ngati mvula yamkuntho imene imawononga mbewu m'munda.

4 Amene amakana malamulo amatamanda anthu oyipa,
koma amene amasunga malamulo amatsutsana nawo.

5 Anthu oyipa samvetsa za chiweruzo cholungama,
koma amene amafuna kuchita zimene Yehova afuna amachimvetsetsa bwino.

6 Munthu wosauka wa makhalidwe abwino
aposa munthu wolemera wa makhalidwe okhotakhota.

7 Amene amasunga malamulo ndi mwana wozindikira zinthu,
koma amene amayenda ndi anthu adyera amachititsa manyazi abambo ake.

8 Amene amachulukitsa chuma chake polandira chiwongoladzanja chochuluka
amakundikira chumacho anthu ena, amene adzachitira chifundo anthu osauka.

9 Wokana kumvera malamulo
ngakhale pemphero lake lomwe limamunyansa Yehova.

10 Amene amatsogolera anthu olungama kuti ayende m'njira yoyipa
adzagwera mu msampha wake womwe,
koma anthu opanda cholakwa adzalandira cholowa chabwino.

11 Munthu wolemera amadziyesa kuti ndi wanzeru,
koma munthu wosauka amene ali ndi nzeru zodziwa zinthu amamutulukira.

12 Pamene olungama apambana pamakhala chikondwerero chachikulu;
koma pamene anthu oyipa apatsidwa ulamuliro, anthu amabisala.

13 Wobisa machimo ake sadzaona mwayi,
koma aliyense amene awulula ndi kuleka machimowo, adzalandira chifundo.

14 Ndi wodala munthu amene amaopa Yehova nthawi zonse,
koma amene aumitsa mtima wake adzagwa m'mavuto.

15 Ngati mkango wobuma kapena chimbalangondo cholusa
ndi mmenenso amakhalira munthu woyipa akamalamulira anthu osauka.

16 Wolamulira amene samvetsa zinthu ndiye amakhala wankhanza
koma amene amadana ndi phindu lopeza mwachinyengo adzakhala ndi moyo wautali.

17 Munthu amene wapalamula mlandu wopha munthu
adzakhala wothawathawa mpaka imfa yake;
wina aliyense asamuthandize.

18 Amene amayenda mokhulupirika adzapulumutsidwa
koma amene njira zake ndi zokhotakhota adzagwa m'dzenje.

19 Amene amalima m'munda mwake adzakhala ndi chakudya chochuluka,
koma amene amangosewera adzakhala m'mphawi.

20 Munthu wokhulupirika adzadalitsika kwambiri,
koma wofuna kulemera mofulumira adzalangidwa.

21 Kukondera si kwabwino,
ena amachita zolakwazo chifukwa cha kachidutswa ka buledi.

22 Munthu wowumira amafunitsitsa kulemera
koma sazindikira kuti umphawi udzamugwera.

23 Amene amadzudzula mnzake potsiriza pake
mnzakeyo adzamukonda kwambiri, kupambana amene amanena mawu oshashalika.

24 Amene amabera abambo ake kapena amayi ake
namanena kuti "kumeneko sikulakwa,"
ndi mnzake wa munthu amene amasakaza.

25 Munthu wadyera amayambitsa mikangano,
koma amene amadalira Yehova adzalemera.

26 Amene amadzidalira yekha ndi chitsiru,
koma amene amatsata nzeru za ena adzapulumuka.

27 Amene amapereka kwa osauka sadzasowa kanthu,
koma amene amatsinzina maso ake adzatemberereredwa kwambiri.

28 Pamene anthu oyipa apatsidwa ulamuliro anthu amabisala,
koma anthu oyipa akawonongeka olungama amapeza bwino.

# 29

1 Munthu amene amawumitsabe khosi lake atadzudzulidwa kwambiri,
adzawonongeka mwadzidzidzi popanda chomuchiritsa.

2 Anthu olungama akamalamulira m'dziko anthu amakondwa,
koma ngati dziko lilamulidwa ndi anthu oyipa mtima anthu amadandaula.

3 Munthu amene amakonda nzeru amasangalatsa abambo ake,
koma woyenda ndi akazi achiwerewere amasakaza chuma chake.

4 Mfumu imalimbitsa dziko poweruza mwachilungamo,
koma mfumu imene imawumiriza anthu kuti ayipatse mphatso imawononga dziko.

5 Munthu woshashalika mnzake,
akudziyalira ukonde mapazi ake.

6 Munthu woyipa amakodwa ndi machimo ake,
koma wochita chilungamo amayimba lokoma.

7 Munthu wolungama amasamalira anthu osauka,
koma woyipa salabadira zimenezi.

8 Anthu onyoza atha kuwutsa ziwawa mu mzinda,
koma anthu anzeru amaletsa ukali.

9 Ngati munthu wanzeru atsutsana ndi chitsiru,
chitsirucho chimachita phokoso ndi kumangoseka ndipo sipakhala mtendere.

10 Anthu okhetsa magazi amadana ndi munthu wangwiro
koma anthu olungama amasamalira moyo wake.

11 Munthu wopusa amaonetsa mkwiyo wake,
koma munthu wanzeru amadzigwira.

12 Ngati wolamulira amvera zabodza,
akuluakulu ake onse adzakhala oyipa.

13 Munthu wosauka ndi munthu wopondereza anzake amafanana pa kuti:
Yehova ndiye anawapatsa maso onsewa.

14 Ngati mfumu iweruza osauka moyenera,
mpando wake waufumu udzakhazikika nthawi zonse.

15 Ndodo ndi chidzudzulo zimapatsa nzeru
koma mwana womulekerera amachititsa amayi ake manyazi.

16 Oyipa akamalamulira zoyipa zimachuluka,
koma anthu olungama adzaona kugwa kwa anthu oyipawo.

17 Umulange mwana wako ndipo adzakupatsa mtendere
ndi kusangalatsa mtima wako.

18 Ngati uthenga wochokera kwa Yehova supezeka anthu amangochita zofuna zawo;
koma wodala ndi amene amasunga malamulo.

19 Munthu wantchito sangalangizidwe ndi mawu okha basi;
ngakhale awamvetse mawuwo sadzatha kuchitapo kanthu.

20 Ngakhale munthu wa uchitsiru n'kuti ndiponi popeza chikhulupiriro chilipo
kuposa munthu wodziyesa yekha kuti ndi wanzeru poyankhula.

21 Ngati munthu asasatitsa wantchito wake kuyambira ali mwana,
potsirizira adzapeza kuti wantchitoyo wasanduka mlowachuma wake.

22 Munthu wamkwiyo amayambitsa mikangano,
ndipo munthu waukali amachita zolakwa zambiri.

23 Kunyada kwa munthu kudzamutsitsa,
koma munthu wodzichepetsa amalandira ulemu.

24 Woyenda ndi munthu wakuba ndi mdani wa moyo wake womwe;
amalumbira koma osawulula kanthu.

25 Kuopa munthu kudzakhala ngati msampha,
koma aliyense amene amadalira Yehova adzatetezedwa.

26 Anthu ambiri amafunitsitsa kuti wolamulira awakomere mtima,
koma munthu amaweruzidwa mwachilungamo ndi thandizo la Yehova basi.

27 Anthu olungama amanyansidwa ndi anthu achinyengo;
koma anthu oyipa amanyansidwa ndi anthu a mtima wowongoka.

# 30

*Mawu a Aguri*

1 Nawa mawu a Aguri mwana wa Yake wa ku Masa:

Munthuyo anati kwa Itieli, "Inu Mulungu, ine ndatopa.
Inu Mulungu, ine ndatopa. Ndalefukiratu.

2 "Ine ndine munthu wopusa kuposa anthu onse;
ndilibe nzeru zomvetsa zinthu zonga za munthu.
3 Sindinaphunzire nzeru,
ndipo Woyerayo sindimudziwa.
4 Kodi ndani anakwera kumwamba ndi kutsikako?
Ndani anafumbatapo mphepo m'manja mwake?
Ndani anamanga madzi m'chovala chake?
Ndani anakhazikitsa mathero onse a dziko lapansi?
Dzina lake ndani? Ndiwuze ngati ukudziwa!
Ndipo mwana wake dzina lake ndani?

5 "Mawu ali wonse a Mulungu ndi opanda cholakwika;
Iye ndi chishango kwa amene amathawira kwa Iye.
6 Usawonjezepo kanthu pa mawu ake,
kuopa kuti Iye angadzakudzudzule ndi kukupeza kuti ndiwe wabodza."

7 "Inu Yehova, ndikukupemphani zinthu ziwiri
musandimane zimenezo ndisanafe:
8 Choyamba, mundichotsere kutali nane mabodza ndi chinyengo.
Chachiwiri, ndisakhale m'mphawi kapena munthu wachuma.
Koma muzindidyetsa chakudya chondikwanira tsiku ndi tsiku
9 kuopa kuti ndikakhuta kwambiri ndingayambe kukukanani,
n'kumanena kuti, 'Yehova ndiye yaninso?'
Kuopanso kuti ndikakhala wosauka ndingayambe kuba,
potero n'kuyipitsa dzina la Mulungu wanga."

10 "Usamusinjirire wantchito kwa mbuye wake
kuopa kuti angakutemberere ndipo iweyo n'kupezeka wolakwa."

11 "Alipo ena amene amatemberera abambo awo,
ndipo sadalitsa amayi awo.
12 Pali ena amene amadziyesa okha oyera mtima
komatu sanachotse zoyipa zawo.
13 Pali ena ndi odzitukumula kwambiri,
amene amakweza zikope modzitukumula.
14 Pali ena amene mano awo ali ngati malupanga
ndipo zibwano zawo zili ngati mipeni
moti amadya amphawi ndi kuwachotsa pa dziko lapansi.
Amachotsanso anthu osauka pakati pa anzawo."

15 "Msundu uli ndi ana aakazi awiri
iwo amalira kuti, 'Tipatseni! Tipatseni!' "

"Pali zinthu zitatu zimene sizikhuta,
zinthu zinayi zimene sizinena kuti, 'Takhuta!'
16 Manda, mkazi wosabala,
nthaka yosakhuta madzi
ndiponso moto womangoyakirayakira!"

17 Aliyense amene amanyoza abambo ake,
ndi kunyozera kumvera amayi ake,
makwangwala a ku chigwa adzamukolowola maso
ndipo mphungu zidzadya mnofu wake.

18 Pali zinthu zitatu zimene zimandidabwitsa,
zinthu zinayi zimene ine sindizimvetsetsa.
19 Ndipo ndi izi: mmene chiwulukira chiwombankhanga mlengalenga;
mmene iyendera njoka pa thanthwe;
mmene chiyendera chombo pa nyanja;
ndiponso mmene mwamuna achitira akakhala ndi namwali.

20 Umu ndi m'mene mkazi amachitira atachita chigololo:
Atatha kudya ndi kupukuta pakamwa pake
iye amanena kuti "Sindinachite kalikonse kolakwa."

21 Pali zinthu zitatu zimene zimanjenjemeretsa dziko lapansi,
pali zinthu zinayi zimene dziko lapansi silingathe kuzipirira:
22 Kapolo amene wasanduka mfumu,
chitsiru chimene chakhuta,
23 mkazi wonyozeka akakwatiwa
ndiponso wantchito wamkazi akalanda mwamuna wa mbuye wake.

24 Pali zinthu zinayi zing'onozing'ono pa dziko lapansi,
komatu ndi zochenjera kwambiri:
25 Nyerere zili ngati anthu opanda mphamvu,
komatu zimasungiratu chakudya chake nthawi ya chilimwe;
26 mbira zili ngati anthu opanda mphamvu
komatu zimakonza pokhalapo pawo m'miyala;
27 dzombe lilibe mfumu,
komatu lonse limakhala m'magulumagulu poyenda.
28 Buluzi ungathe kumugwira m'manja
komatu amapezeka m'nyumba za mafumu.

29 "Pali zinthu zitatu zimene zimayenda chinyachinya,
pali zinthu zinayi zimene zimayenda monyadira:
30 Mkango umene uli wamphamvu kuposa nyama zonse,
ndipo suthawa kanthu kalikonse.
31 Tambala woyenda chinyachinya, mbuzi yayimuna,
ndiponso mfumu yoyenda pakati pa anthu ake.

32 "Ngati wakhala ukupusa ndi kumadzikweza wekha,
kapena ngati wakhala ukukonzekera zoyipa,
ndiye khala kaye chete, uganizire bwino!
33 Paja pakutha mkaka mafuta amapangidwa,
ndipo ukapsinya mphuno, magazi amatuluka,
ndipo mikangano imakhalapo ukalimbikira kukwiya."

# 31

*Mawu a Mfumu Lemueli*

[1] Nawa mawu a mfumu Lemueli wa ku Massa amene anamuphunzitsa amayi ake:
[2] N'chiyani mwana wanga? N'chiyani mwana wa m'mimba mwanga?
N'chiyani iwe mwana wanga amene ndinachita kupempha ndi malumbiro?
[3] Usapereke mphamvu yako kwa akazi.
Usamayenda nawo amenewa popeza amawononga ngakhale mafumu.

[4] Iwe Lemueli si choyenera kwa mafumu,
mafumu sayenera kumwa vinyo.
Olamulira asamalakalake chakumwa choledzeretsa
[5] kuopa kuti akamwa adzayiwala malamulo a dziko,
nayamba kukhotetsa zinthu zoyenera anthu osauka.
[6] Perekani chakumwa choledzeretsa kwa amene ali pafupi kufa,
vinyo kwa amene ali pa mavuto woopsa;
[7] amwe kuti ayiwale umphawi wawo
asakumbukirenso kuvutika kwawo.

[8] Yankhula m'malo mwa amene sangathe kudziyankhulira okha.
Uwayankhulire anthu onse osiyidwa pa zonse zowayenera.
[9] Yankhula ndi kuweruza mwachilungamo.
Uwateteze amphawi ndi osauka.

*Mathero: Mkazi Wangwiro*

[10] Kodi mkazi wangwiro angathe kumupeza ndani?
Ndi wokwera mtengo kuposa miyala yamtengowapatali.
[11] Mtima wa mwamuna wake umamukhulupirira
ndipo mwamunayo sasowa phindu.
[12] Masiku onse a moyo wake
mkaziyo amachitira mwamuna wake zabwino zokhazokha osati zoyipa.
[13] Iye amafunafuna ubweya ndi thonje;
amagwira ntchito ndi manja ake mwaufulu.
[14] Iye ali ngati sitima zapamadzi za anthu amalonda,
amakatenga chakudya chake kutali.
[15] Iye amadzuka kusanache kwenikweni;
ndi kuyamba kukonzera a pa banja pake chakudya
ndi kuwagawira ntchito atsikana ake antchito.
[16] Iye amalingalira za munda ndi kuwugula;
ndi ndalama zimene wazipeza amalima munda wamphesa.
[17] Iye amavala zilimbe
nagwira ntchito mwamphamvu ndi manja ake.
[18] Iye amaona kuti malonda ake ndi aphindu,
choncho nyale yake sizima usiku wonse.
[19] Iye amadzilukira thonje
ndipo yekha amagwira chowombera nsalu.
[20] Iye amachitira chifundo anthu osauka
ndipo amapereka chithandizo kwa anthu osowa.
[21] Iye saopa kuti banja lake lifa ndi kuzizira pa nyengo yachisanu;
pakuti onse amakhala atavala zovala zofunda.
[22] Iye amadzipangira yekha zoyala pa bedi pake;
amavala zovala zabafuta ndi zapepo.

23 Mwamuna wake ndi wodziwika pa chipata cha mzinda,
ndipo amakhala pakati pa akuluakulu a m’dzikomo.
24 Iye amasoka nsalu zabafuta nazigulitsa;
amaperekanso mipango kwa anthu amalonda.
25 Mphamvu ndi ulemu zimakhala ngati chovala chake;
ndipo amaseka osaopa zam’tsogolo.
26 Iye amayankhula mwanzeru,
amaphunzitsa anthu mwachikondi.
27 Iye amayang’anira makhalidwe a anthu a pa banja lake
ndipo sachita ulesi ndi pang’ono pomwe.
28 Ana ake amamunyadira ndipo amamutcha kuti wodala;
ndipo mwamuna wake, amamuyamikira n’kumati,
29 “Pali akazi ambiri amene achita zinthu zopambana
koma iwe umawaposa onsewa.”
30 Nkhope yachikoka ndi yonyenga, ndipo kukongola n’kosakhalitsa;
koma mkazi amene amaopa Yehova ayenera kutamandidwa.
31 Mupatseni mphotho chifukwa cha zimene iye wachita
ndipo ntchito zake zimutamande ku mabwalo.

# Mlaliki

*Zapansipano N'zopandapake*

1 Mawu a Mlaliki, mwana wa Davide, mfumu ya ku Yerusalemu:
2 "Zopandapake! Zopandapake!"
atero Mlaliki.
"Zopandapake kotheratu!
Zopandapake."

3 Kodi munthu amapindulanji pa ntchito zake zonse
zimene amasautsidwa nazo pansi pano?
4 Mibado imabwera ndipo mibado imapita,
koma dziko lapansi limakhalapobe nthawi zonse.
5 Dzuwa limatuluka ndipo dzuwa limalowa
ndipo limapita mwamsanga kumene limatulukira.
6 Mphepo imawombera cha kummwera
ndi kukhotera cha kumpoto;
imawomba mozungulirazungulira,
kumangobwererabwerera komwe yachokera.
7 Mitsinje yonse imakathira ku nyanja,
koma nyanjayo sidzaza;
kumene madziwo amachokera,
amabwerera kumweko.
8 Zinthu zonse ndi zotopetsa,
kutopetsa kwake ndi kosaneneka.
Maso satopa ndi kuona
kapena khutu kukwaniritsidwa ndi kumva.
9 Zomwe zinalipo kale zidzakhalaponso,
zomwe zinachitika kale zidzachitikanso.
Ndiye kuti chatsopano palibiretu pansi pano.
10 Kodi chilipo chinthu chimene wina anganene kuti,
"Taona! Ichi ndiye chatsopano?"
Chinalipo kale, kalekale;
chinalipo ife kulibe.
11 Anthu akale sakumbukiridwa,
ngakhale amene adzabwera m'tsogolomu
sadzakumbukiridwa ndi iwo
amene adzabwere pambuyo pawo.

*Nzeru N'zopandapake*

12 Ine, Mlalikine, ndinali mfumu ya Israeli mu Yerusalemu. 13 Ndinayika
mtima wanga pophunzira ndi kufunafuna mwa nzeru zinthu zonse
zimene zimachitika pansi pa thambo. Ndi ntchito yolemetsa ndithu imene
Mulungu anayipereka kwa anthu! 14 Ine ndaona zinthu zonse zochitika
pansi pano; zinthu zonsezo ndi zopandapake, n'kungodzivuta chabe.
15 Chinthu chokhota sichingathe kuwongoledwa;
chimene palibe sichingathe kuwerengedwa.
16 Ine ndinaganiza mu mtima mwanga, "Taona, ine ndakula ndi
kukhala wa nzeru zochuluka kupambana aliyense amene analamulirapo
Yerusalemu ndisanabadwe; ndaphunzira nzeru zochuluka ndi luntha."

17 Ndipo ndinadzipereka kuti ndithe kumvetsa kuti nzeru n'chiyani, misala n'chiyani, uchitsiru n'chiyani, koma ndinazindikira ichi, kuti kuteronso n'kungodzivuta chabe.

18 Pakuti nzeru zochuluka zimabweretsa chisoni chochulukanso:
chidziwitso chochuluka, zowawa zochulukanso.

# 2

*Zosangalatsa N'zopandapake*

1 Ine ndinaganiza mu mtima mwanga, "Tsopano ndiyese zosangalatsa
kuti ndipeze zomwe ndi zabwino." Koma izi zinaonekanso kuti ndi
zopandapake. 2 "Kuseka," ndinati, "imeneyo ndi misala. Ndipo kodi
chisangalalo chimabweretsa phindu lanji?" 3 Ndinayesa kudzisangalatsa
ndi vinyo, koma umenewu unali uchitsiru, pamenepo n'kuti maganizo anga akutsogozedwa ndi nzeru. Ine ndinkati mwina kapena njira yotero n'kukhala yopambana, imene anthu amatsata pofuna kusangalala pa masiku owerengeka a moyo wawo.

4 Ndinagwira ntchito zikuluzikulu: Ndinadzimangira nyumba ndi
kuwoka mipesa. 5 Ndinalima madimba ndi minda yamitengo; ndipo
ndinadzalamo mitengo ya zipatso za mitundu yonse. 6 Ndinakumba
mayiwe osungiramo madzi woti ndizithirira minda ya mitengo yodzalidwa
ija. 7 Ndinagula akapolo aamuna ndi akapolo aakazi, ndiponso ndinali
ndi akapolo ena omwe anabadwira m'nyumba mwanga. Ndinalinso ndi ng'ombe ndi nkhosa zambiri kupambana aliyense mu Yerusalemu amene
analipo ndisanabadwe. 8 Ndinadzikundikira siliva ndi golide, ndiponso
chuma chochokera kwa mafumu ndi madera awo. Ndinali ndi amuna ndi akazi oyimba ndiponso azikazi; zinthu zokondweretsa mtima wa munthu.
9 Ndinali munthu wotchuka kupambana wina aliyense mu Yerusalemu
amene analipo ndisanabadwe. Mu zonsezi nzeru zanga zinali nane.

10 Sindinadzimane chilichonse chimene maso anga anachifuna;
mtima wanga sindinawumane zokondweretsa.
Mtima wanga unakondwera ndi ntchito yanga yonse,
ndipo iyi ndiyo inali mphotho ya ntchito zanga zonse zolemetsa.
11 Koma pamene ndinayamba kuyang'anayang'ana zonse zimene ndinachita ndi manja anga,
ndi zimene ndinazivutikira kuti ndizipeze,
zonsezi zinali zopandapake; kungodzivuta chabe,
palibe chomwe ndinapindula pansi pano.

*Nzeru ndi Uchitsiru N'zopandapake*

12 Kenaka maganizo anga anayamba kulingalira zakuti nzeru n'chiyani,
komanso kuti misala ndi uchitsiru n'chiyani.
Kodi munthu wodzalowa ufumu tsopanoyo angachite chiyani
choposa chimene chinachitidwa kale?
13 Ndinaona kuti nzeru ndi yopambana uchitsiru,
monga momwe kuwala kumapambanira mdima.
14 Munthu wanzeru amayenda maso ali patsogolo,
pamene chitsiru chimayenda m'chimbulimbuli;
koma ndinazindikira kuti chomwe
chimawachitikira onsewo ndi chimodzi.
15 Pamenepo ndinalingalira mu mtima mwanga,
"Zochitikira chitsiru zidzandichitikiranso ine.
Nanga tsono phindu langa n'chiyani pakukhala wanzeru?"

Ndinati mu mtima mwanga,
“Ichinso ndi chopandapake.”
16 Pakuti munthu wanzeru, pamodzinso ndi chitsiru sadzakumbukiridwa
nthawi yayitali;
m’masiku am’tsogolo awiriwo adzayiwalika.
Mmene chimafera chitsiru ndi mmenenso amafera wanzeru!

*Kugwira Ntchito N’kopandapake*

17 Kotero ndinadana nawo moyo chifukwa ntchito zimene zimagwiridwa
pansi pano ndi zosautsa kwa ine. Ntchito zonsezo ndi zopandapake,
n’kungodzivuta chabe. 18 Ine ndinadana nazo ntchito zonse zimene
ndinazigwira pansi pano, chifukwa ndinayenera kudzazisiyira wina
amene adzalowa m’malo mwanga. 19 Ndipo ndani amadziwa kuti munthu
ameneyo adzakhala wanzeru kapena chitsiru? Komabe munthuyo
adzakhala wolamulira zonse zimene ndinazichita pansi pano mwa nzeru
zanga. Izinso ndi zopandapake. 20 Motero ndinayamba kutaya mtima
chifukwa cha ntchito zonse zimene ndinazivutikira pansi pano. 21 Pakuti
munthu atha kugwira ntchito yake mwanzeru, chidziwitso ndi luntha,
ndipo kenaka n’kusiyira wina amene sanakhetserepo thukuta. Izinso ndi
zopandapake ndiponso tsoka lalikulu. 22 Kodi munthu amapindulanji pa
ntchito zonse zolemetsa ndi zodetsa nkhawa zimene amazichita pansi
pano? 23 Masiku ake onse amakhala achisoni, ntchito yake imakhala
yovuta; ngakhale usiku womwe, mtima wake supumula. Izinso ndi
zopandapake.
24 Kwa munthu palibe chabwino china kuposa kudya, kumwa ndi
kukondwerera ntchito zake. Izinso ndaona kuti ndi zochokera kwa
Mulungu, 25 pakuti popanda Iye, ndani angadye ndi kupeza chisan-
galalo? 26 Munthu amene amakondweretsa Mulungu, Mulunguyo ama-
musandutsa wanzeru, wozindikira ndi wachisangalalo, koma wochimwa,
Mulungu amamupatsa ntchito yosonkhanitsa ndi kusunga chuma kuti
adzachipereke kwa amene Mulunguyo amakondwera naye. Izinso ndi
zopandapake, n’kungodzivuta chabe.

# 3

*Chilichonse Chili ndi Nthawi*

1 Chinthu chilichonse chili ndi nthawi yake,
ndi nyengo yake yomwe anayika Mulungu:

2 Nthawi yobadwa ndi nthawi yomwalira,
nthawi yodzala ndi nthawi yokolola.
3 Nthawi yakupha ndi nthawi yochiritsa,
nthawi yogwetsa ndi nthawi yomanga.
4 Nthawi yomva chisoni ndi nthawi yosangalala,
nthawi yolira maliro ndi nthawi yovina.
5 Nthawi yotaya miyala ndi nthawi yokundika miyala,
nthawi yokumbatirana ndi nthawi yoleka kukumbatirana.
6 Nthawi yofunafuna ndi nthawi yoleka kufunafuna,
nthawi yosunga ndi nthawi yotaya.
7 Nthawi yong’amba ndi nthawi yosoka,
nthawi yokhala chete ndi nthawi yoyankhula.
8 Nthawi yokondana ndi nthawi yodana,
nthawi ya nkhondo ndi nthawi ya mtendere.

9 Kodi wantchito amapeza phindu lanji pa ntchito yake yolemetsa?
10 Ine ndinaona chipsinjo chimene Mulungu anayika pa anthu. 11 Iye
anapanga chinthu chilichonse kuti chikhale chabwino pa nthawi yake.
Anayika nzeru zamuyaya m'mitima ya anthu; komabe anthuwo sangathe
kuzindikira zomwe Mulungu wachita kuyambira pa chiyambi mpaka
chimaliziro. 12 Ine ndikudziwa kuti palibenso kanthu kabwino kwa
anthu kopambana kusangalala ndi kuchita zabwino pamene ali ndi moyo.
13 Ndi mphatso ya Mulungu kwa munthu kuti azidya, azimwa ndi ku-
makondwera ndi ntchito zake zolemetsa. 14 Ndikudziwa kuti chilichonse
chimene Mulungu amachita chidzakhala mpaka muyaya; palibe zimene
zingawonjezedwe kapena kuchotsedwa. Mulungu amazichita kuti anthu
azimuopa.

15 Chilichonse chimene chilipo chinalipo kale,
ndipo chimene chidzakhalapo chinalipo poyamba;
Mulungu amabwezanso zakale zimene zinapita kuti zichitikenso.

16 Ndipo ndinaona chinthu chinanso pansi pano:
ku malo achiweruzo, kuyipa mtima kuli komweko,
ku malo achilungamo, kuyipa mtima kuli komweko.

17 Ndinalingalira mu mtima mwanga kuti;
"Mulungu adzaweruza
olungama pamodzi ndi oyipa omwe,
pakuti anayika nthawi yochitikira chinthu chilichonse,
nthawi ya ntchito iliyonse."

18 Ndinalingaliranso kuti, "Kunena za anthu, Mulungu amawayesa ndi
cholinga choti awaonetse kuti iwo ali ngati nyama. 19 Zimene zima-
chitikira munthu, zomwezonso zimachitikira nyama; chinthu chimodzi
chomwecho chimachitikira onse: Monga munthu amafa momwemonso
nyama imafa. Zonsezi zimapuma mpweya umodzimodzi omwewo;
munthu saposa nyama. Zonsezi ndi zopandapake. 20 Zonse zimapita
kumodzimodzi; zonsezi zimachokera ku fumbi, ndipo zimabwerera nso ku
fumbi komweko. 21 Kodi ndani amene amadziwa ngati mzimu wa munthu
umakwera kumwamba, ndipo mzimu wa nyama umatsikira kunsi kwa
dziko?"

22 Kotero ndinaona kuti palibe chinthu chabwino kwa munthu kuposa
kuti munthu azisangalala ndi ntchito yake, pakuti ichi ndiye chake
chenicheni. Pakuti ndani amene angamubweretse kuti adzaone zimene
zidzamuchitikira iye akadzamwalira?

# 4

*Matsoka ndi Mavuto a Moyo Uno*

1 Ndinayang'ananso ndi kuona chipsinjo chimene chimachitika pansi
pano:
ndinaona misozi ya anthu opsinjika,
ndipo iwo alibe owatonthoza;
mphamvu zinali ndi anthu owapsinjawo
ndipo iwonso analibe owatonthoza.

2 Ndipo ndinanena kuti akufa,
amene anafa kale,
ndi osangalala kuposa amoyo,
amene akanalibe ndi moyo.

3 Koma wopambana onsewa
ndi amene sanabadwe,

amene sanaone zoyipa
zimene chimachitika pansi pano.
4 Ndipo ndinazindikira kuti ntchito zonse zolemetsa ndiponso ntchito
zonse zaluso zimachitika chifukwa choti wina akuchitira nsanje mnzake.
Izinso ndi zopandapake, n'kungodzivuta chabe.
5 Chitsiru chimangoti manja ake lobodo
ndi kudzipha chokha ndi njala.
6 N'kwabwino kukhala ndi dzanja limodzi lodzaza uli pa mtendere,
kuposa kukhala ndi manja awiri odzaza uli pa mavuto,
ndipo uku n'kungodzivuta chabe.
7 Ndinaonanso chinthu china chopanda phindu pansi pano:
8 Panali munthu amene anali yekhayekha;
analibe mwana kapena m'bale.
Ntchito yake yolemetsa sinkatha,
ndipo maso ake sankakhutitsidwa ndi chuma chake.
Iye anadzifunsa kuti, "Kodi ntchito yosautsayi ndikuyigwirira yani?
Nanga n'chifukwa chiyani ndikudzimana chisangalalo?"
Izinso ndi zopandapake,
zosasangalatsa!

9 Kukhala awiri n'kwabwino kuposa kukhala wekha,
chifukwa ntchito ya anthu awiri ili ndi phindu:
10 Ngati winayo agwa,
mnzakeyo adzamudzutsa.
Koma tsoka kwa munthu amene agwa
ndipo alibe wina woti amudzutse!
11 Komanso ngati anthu awiri agona malo amodzi, adzafunditsana.
Koma nanga mmodzi angadzifunditse yekha?
12 Munthu mmodzi angathe kugonjetsedwa,
koma anthu awiri akhoza kudziteteza.
Chingwe cha maulusi atatu sichidukirapo.

*Kutukuka N'kopandapake*

13 Wachinyamata wosauka koma wanzeru aposa mfumu yokalamba
koma yopusa imene simvanso malangizo. 14 Wachinyamatayo angathe
kuchokera ku ndende ndi kudzakhala mfumu, kapena angathe kubadwa
wosauka m'dziko la mfumuyo. 15 Ndipo ndinaona kuti iwo onse amene
anakhala ndi moyo ndi kuyenda pansi pano anatsatira wachinyamatayo,
amene anatenga malo a mfumu. 16 Mfumu ikhoza kulamulira anthu
osawerengeka, komabe itamwalira, palibe amene adzayamikire zomwe
mfumuyo inachita. Izinso ndi zopandapake, n'kungozivuta chabe.

# 5

*Lemekeza Mulungu*

1 Uzisamala mayendedwe ako pamene ukupita ku nyumba ya Mulungu.
Upite pafupi kuti ukamvetsere m'malo mopereka nsembe ya zitsiru
zimene sizizindikira kuti zikuchita zolakwa.
2 Usamafulumire kuyankhula,
usafulumire mu mtima mwako
kunena chilichonse pamaso pa Mulungu.
Mulungu ali kumwamba

ndipo iwe uli pa dziko lapansi,
choncho mawu ako akhale ochepa.
3 Kuchuluka kwa mavuto mu mtima kumabweretsa maloto oyipa,
ndipo kuchuluka kwa mawu kumadzetsa uchitsiru.
4 Pamene ulumbira kwa Mulungu usachedwe kukwaniritsa chimene
walumbiracho. Iye sakondweretsedwa ndi chitsiru; kwaniritsa lumbiro
lako. 5 Kuli bwino kusalumbira kusiyana ndi kulumbira koma osakwanir-
itsa lumbirolo. 6 Pakamwa pako pasakuchimwitse. Ndipo usanene kwa
mthenga wa m'Nyumba ya Mulungu kuti, "Ndinalakwitsa polumbira."
Chifukwa chiyani ukufuna Mulungu akwiye ndi mawu ako ndiponso
ntchito ya manja ako? 7 Maloto ochuluka ndi mawu ochuluka ndi zinthu
zopandapake. Kotero lemekeza Mulungu.

### *Chuma N'chopandapake*

8 Ngati uwona anthu osauka akuzunzika m'dziko, ndiponso anthu ena
akupsinja anzawo ndi kuwalanda ufulu wawo, usadabwe ndi zinthu
zimenezi; pakuti woyang'anira ali naye wina womuyang'anira wamkulu,
ndipo pamwamba pa awiriwa pali ena akuluakulu owaposa. 9 Anthu onse
amatengako zokolola za m'minda: koma ndi mfumu yokha imene imapeza
phindu la mindayi.
10 Aliyense amene amakonda ndalama sakhutitsidwa ndi ndalamazo;
aliyense amene amakonda chuma sakhutitsidwa ndi zimene amapeza.
Izinso ndi zopandapake.

11 Chuma chikachuluka
akudya nawo chumacho amachulukanso.
Nanga mwini wake amapindulapo chiyani
kuposa kumangochiyang'ana ndi maso ake?

12 Wantchito amagona tulo tabwino
ngakhale adye pang'ono kapena kudya kwambiri,
koma munthu wolemera, chuma
sichimulola kuti agone.
13 Ine ndinaona choyipa chomvetsa chisoni pansi pano:
chuma chokundikidwa chikupweteka mwini wake yemwe,
14 kapena chuma chowonongedwa pa nthawi yatsoka,
kotero kuti pamene wabereka mwana
alibe kanthu koti amusiyire.
15 Munthu anabadwa wamaliseche kuchokera m'mimba mwa amayi ake,
ndipo monga iye anabadwira, adzapitanso choncho.
Pa zonse zimene iye anakhetsera thukuta
palibe n'chimodzi chomwe chimene adzatenge m'manja mwake.
16 Izinso ndi zoyipa kwambiri:
munthu adzapita monga momwe anabwerera,
ndipo iye amapindula chiyani,
pakuti amagwira ntchito yolemetsa yopanda phindu?
17 Masiku ake onse ndi odzaza ndi mdima,
kukhumudwa kwakukulu, masautso ndi nkhawa.
18 Tsono ndinazindikira kuti n'chabwino ndi choyenera kuti munthu
azidya ndi kumwa, ndi kukhutitsidwa ndi ntchito yake yolemetsa imene
amayigwira pansi pano pa nthawi yake yochepa imene Mulungu amamu-
patsa, poti ichi ndiye chake. 19 Komatu pamene Mulungu apereka chuma

kwa munthu aliyense ndi zinthu zina, ndi kulola kuti akondwere ndi
chumacho, munthuyo alandire chumacho ndi kusangalala ndi ntchito
yake, imene ndi mphatso yochokera kwa Mulungu. 20 Munthu wotereyu
saganizirapo za masiku a moyo wake, chifukwa Mulungu amamutanganid-
witsa ndi chisangalalo cha mu mtima mwake.

# 6

1 Ine ndinaona choyipa china pansi pano, ndipo chimasautsa anthu
kwambiri: 2 Mulungu amapereka chuma, zinthu ndi ulemu kwa munthu,
kotero kuti munthuyo sasowa kanthu kalikonse kamene akukalakalaka,
koma Mulungu samulola kuti adyerere zinthuzo, ndipo m'malo mwake
amadyerera ndi mlendo. Izi ndi zopandapake, ndi zoyipa kwambiri.
3 Ngakhale munthu atabereka ana 100 ndi kukhala ndi moyo zaka
zambiri; komatu ngakhale atakhala zaka zambiri chotani, ngati iye san-
gadyerere chuma chake ndi kuyikidwa m'manda mwaulemu, ine ndikuti
mtayo umamuposa iyeyo. 4 Mtayo umangopita pachabe ndipo umapita
mu mdima, ndipo mu mdimamo dzina lake limayiwalika. 5 Ngakhale
kuti mtayowo sunaone dzuwa kapena kudziwa kanthu kalikonse, koma
umapumula kuposa munthu uja, 6 ngakhale munthuyo atakhala ndi moyo
zaka 2,000, koma ndi kulephera kudyerera chuma chake. Kodi onsewa
sapita malo amodzi?

7 Ntchito yonse ya munthu imathera pakamwa pake,
komatu iye sakhutitsidwa ndi pang'ono pomwe.
8 Kodi munthu wanzeru
amaposa motani chitsiru?
Kodi munthu wosauka amapindula chiyani
podziwa kukhala bwino pamaso pa anthu ena?
9 Kuli bwino kumangoona zinthu ndi maso
kusiyana ndi kumangozilakalaka mu mtima.
Izinso ndi zopandapake,
n'kungodzivuta chabe.

10 Chilichonse chimene chilipo anachitchula kale dzina,
za mmene munthu alili n'zodziwika;
sangathe kutsutsana ndi munthu
amene ali wamphamvu kupambana iyeyo.
11 Mawu akachuluka
zopandapake zimachulukanso,
nanga munthu zimamupindulira chiyani?

12 Pakuti ndani amene amadziwa chomwe ndi chabwino pa moyo wa
munthu, pakuti moyo wake ndi wa masiku ochepa ndi opandapake,
umangopitira ngati mthunzi. Ndani amene angamufotokozere zimene
zidzachitika pansi pano iye atapita?

# 7

*Nzeru*

1 Mbiri yabwino ndi yopambana mafuta onunkhira bwino,
ndipo tsiku lomwalira ndi lopambana tsiku lobadwa.
2 Kuli bwino kupita ku nyumba yamaliro
kusiyana ndi kupita ku nyumba yamadyerero:
Pakuti imfa ndiye mathero a munthu aliyense;
anthu amoyo azichisunga chimenechi m'mitima mwawo.

3 Chisoni n'chabwino kusiyana ndi kuseka,
pakuti nkhope yakugwa ndi yabwino chifukwa imakonza mtima.
4 Mtima wa munthu wanzeru nthawi zonse umalingalira za imfa,
koma mitima ya zitsiru imalingalira za chisangalalo.
5 Kuli bwino kumva kudzudzula kwa munthu wanzeru
kusiyana ndi kumvera mayamiko a zitsiru.
6 Kuseka kwa zitsiru kuli ngati
kuthetheka kwa moto kunsi kwa m'phika,
izinso ndi zopandapake.

7 Kuzunza ena kumasandutsa munthu wanzeru kukhala chitsiru,
ndipo chiphuphu chimawononga mtima.

8 Mathero ake a chinthu ndi abwino kupambana chiyambi chake,
ndipo kufatsa n'kwabwino kupambana kudzikuza.
9 Usamafulumire kukwiya mu mtima mwako,
pakuti mkwiyo ndi bwenzi la zitsiru.

10 Usamafunse kuti, "N'chifukwa chiyani masiku amakedzana anali abwino kupambana masiku ano?"
pakuti si chinthu chanzeru kufunsa mafunso oterewa.

11 Nzeru ngati cholowa, ndi chinthu chabwino
ndipo imapindulitsa wamoyo aliyense pansi pano.
12 Nzeru ndi chitetezo,
monganso ndalama zili chitetezo,
koma phindu la chidziwitso ndi ili:
kuti nzeru zimasunga moyo wa munthu amene ali nazo nzeruzo.
13 Taganizirani zimene Mulungu wazichita:
ndani angathe kuwongola chinthu
chimene Iye anachipanga chokhota?
14 Pamene zinthu zili bwino, sangalala;
koma pamene zinthu sizili bwino, ganizira bwino:
Mulungu ndiye anapanga nthawi yabwinoyo,
ndiponso nthawi imene si yabwinoyo.
Choncho munthu sangathe kuzindikira
chilichonse cha m'tsogolo mwake.
15 Pa moyo wanga wopanda phinduwu ndaona zinthu ziwiri izi:
munthu wolungama akuwonongeka m'chilungamo chake,
ndipo munthu woyipa akukhala moyo wautali m'zoyipa zake.
16 Usakhale wolungama kwambiri
kapena wanzeru kwambiri,
udziwonongerenji wekha?
17 Usakhale woyipa kwambiri,
ndipo usakhale chitsiru,
uferenji nthawi yako isanakwane?
18 N'kwabwino kuti utsate njira imodzi,
ndipo usataye njira inayo.
Munthu amene amaopa Mulungu adzapewa zinthu ziwiri zonsezi.

19 Nzeru zimapereka mphamvu zambiri kwa munthu wanzeru
kupambana olamulira khumi a mu mzinda.

20 Palibe munthu wolungama pa dziko lapansi
amene amachita zabwino zokhazokha ndipo sachimwa.

21 Usamamvetsere mawu onse amene anthu amayankhula,
mwina udzamva wantchito wako akukutukwana,
22 pakuti iwe ukudziwa mu mtima mwako
kuti nthawi zambiri iwenso unatukwanapo ena.
23 Zonsezi ndinaziyesa ndi nzeru zanga ndipo ndinati,
"Ine ndatsimikiza mu mtima mwanga kuti ndikhale wanzeru,"
koma nzeruyo inanditalikira.
24 Nzeru zimene zilipo,
zili kutali ndipo ndi zozama kwambiri,
ndani angathe kuzidziwa?
25 Kotero ndinayikapo mtima wanga kuti ndidziwe,
ndifufuze ndi kumafunafuna nzeru ndi mmene zinthu zimakhalira
ndipo ndinafunanso kudziwa kuyipa kwa uchitsiru
ndiponso kupusa kwake kwa misala.

26 Ndinapeza kanthu kowawa kupambana imfa,
mkazi amene ali ngati khoka,
amene mtima wake uli ngati khwekhwe,
ndipo manja ake ali ngati maunyolo.
Munthu amene amakondweretsa Mulungu adzathawa mkaziyo,
koma mkaziyo adzakola munthu wochimwa.
27 Mlaliki akunena kuti, "Taonani, chimene ndinachipeza ndi ichi:
"Kuwonjezera chinthu china pa china kuti ndidziwe mmene zinthu zimachitikira,
28 pamene ine ndinali kufufuzabe
koma osapeza kanthu,
ndinapeza munthu mmodzi wolungama pakati pa anthu 1,000,
koma pakati pawo panalibepo mkazi mmodzi wolungama.
29 Chokhacho chimene ndinachipeza ndi ichi:
Mulungu analenga munthu, anamupatsa mtima wolungama,
koma anthu anatsatira njira zawozawo zambirimbiri."

# 8

1 Ndani angafanane ndi munthu wanzeru?
Ndani angadziwe kutanthauzira zinthu?
Nzeru imabweretsa chimwemwe pa nkhope ya munthu
ndipo imasintha maonekedwe ake awukali.

*Za Kumvera Mfumu*

2 Ine ndikuti, mvera lamulo la mfumu, chifukwa unalumbira pamaso
pa Mulungu. 3 Usafulumire kuchoka pamaso pa mfumu. Usawumirire
chinthu choyipa, pakuti mfumu idzachita chilichonse chomwe imasan-
galatsidwa nacho. 4 Popeza mawu a mfumu ali ndi mphamvu, ndani
anganene kwa mfumuyo kuti, "Kodi mukuchita chiyani?"
5 Aliyense amene amamvera lamulo lake sadzapeza vuto lililonse,
ndipo munthu wanzeru amadziwa nthawi yoyenera ndi machitidwe ake.
6 Pakuti pali nthawi yoyenera ndiponso machitidwe a chinthu chilichonse,
ngakhale kuti mavuto ake a munthu amupsinja kwambiri.

7 Popeza palibe munthu amene amadziwa zam'tsogolo,
ndani angamuwuze zomwe zidzachitika m'tsogolo?
8 Palibe munthu amene ali ndi mphamvu yolamulira mpweya wa moyo
kuti athe kuwusunga,
choncho palibe amene ali ndi mphamvu pa tsiku la imfa yake.
Nkhondo sithawika; tsono anthu ochita zoyipa,
kuyipa kwawoko sikudzawapulumutsa.

9 Zonsezi ndinaziona pamene ndinalingalira mu mtima mwanga, zonse
zimene zimachitika pansi pano. Ilipo nthawi imene ena amalamulira
anzawo mwankhanza. 10 Kenaka, ndinaona anthu oyipa akuyikidwa
m'manda, iwo amene ankalowa ndi kumatuluka m'malo opatulika ndipo
ankatamandidwa mu mzindawo pamene ankachita zimenezi. Izinso ndi
zopandapake.

11 Pamene chigamulo cha anthu opalamula mlandu chikuchedwa,
mitima ya anthu imadzaza ndi malingaliro ochita zolakwa. 12 Ngakhale
munthu woyipa apalamule milandu yambirimbiri, n'kumakhalabe ndi
moyo wautali, ine ndikudziwa kuti anthu owopa Mulungu zinthu zidza-
wayendera bwino, omwe amapereka ulemu pamaso pa Mulungu. 13 Koma
popeza oyipa saopa Mulungu zinthu sizidzawayendera bwino, ndipo moyo
wawo sudzakhalitsa monga mthunzi.

14 Palinso chinthu china chopanda phindu chomwe chimachitika pa
dziko lapansi: anthu olungama amalangidwa ngati anthu osalungama.
Pamene oyipa amalandira zabwino ngati kuti ndi anthu abwino.
15 N'chifukwa chake ndikuti munthu azikondwerera moyo, pakuti munthu
alibe chinanso chabwino pansi pano choposa kudya, kumwa ndi ku-
madzikondweretsa. Akamatero, munthuyo adzakhala ndi chimwemwe pa
ntchito yake masiku onse a moyo wake amene Mulungu wamupatsa pansi
pano.

16 Pamene ndinayikapo mtima wanga kuti ndidziwe nzeru ndi kuonet-
setsa ntchito za munthu pa dziko lapansi, osapeza tulo usana ndi
usiku, 17 pamenepo ndinaona zonse zimene Mulungu anazichita. Palibe
munthu amene angathe kuzimvetsa zonse zimene zimachitika pansi
pano. Ngakhale munthu ayesetse kuzifufuza, sangathe kupeza tanthauzo
lake. Ngakhale munthu wanzeru atanena kuti iye amadziwa, sangathe
kuzimvetsetsa zinthuzo.

# 9

### *Mathero a Zinthu Zonse ndi Wofanana*

1 Ndinalingalira zonse ndanenazi ndipo ndinapeza kuti anthu olungama
ndi anthu anzeru ali m'manja mwa Mulungu pamodzi ndi zimene
amachita, koma palibe amene amadziwa zimene zikumudikira m'tsogolo
mwake, kaya chikondi kapena chidani. 2 Onsewa mathero awo ndi
amodzi, anthu olungama ndi anthu oyipa, abwino ndi oyipa, oyera ndi
odetsedwa, amene amapereka nsembe ndi amene sapereka nsembe.
Zomwe zimachitikira munthu wabwino,
zimachitikiranso munthu wochimwa,
zomwe zimachitikira amene amalumbira,
zimachitikiranso amene amaopa kulumbira.

3 Choyipa chimene chili m'zonse zochitika pansi ndi ichi: Mathero a
zonse ndi amodzi. Ndithu, mitima ya anthu ndi yodzaza ndi zoyipa, ndipo
m'mitima mwawo muli zamisala pamene ali ndi moyo, potsiriza pake iwo

amakakhala pamodzi ndi anthu akufa. 4 Aliyense amene ali ndi moyo
amakhala ndi chiyembekezo, pajatu galu wamoyo aposa mkango wakufa!
5 Pakuti amoyo amadziwa kuti adzafa,
koma akufa sadziwa kanthu;
alibe mphotho ina yowonjezera,
ndipo palibe amene amawakumbukira.
6 Chikondi chawo, chidani chawo
ndiponso nsanje yawo, zonse zinatha kalekale;
sadzakhalanso ndi gawo
pa zonse zochitika pansi pano.
7 Pita, kadye chakudya chako mokondwera ndi kumwa vinyo wako ndi
mtima wosangalala, pakuti tsopano Mulungu akukondwera ndi zochita
zako. 8 Uzivala zovala zoyera nthawi zonse, uzidzola mafuta m'mutu
mwako nthawi zonse. 9 Uzikondwerera moyo pamodzi ndi mkazi wako
amene umamukonda, masiku onse a moyo uno wopanda phindu, amene
Mulungu wakupatsa pansi pano. Pakuti mkaziyo ndiye gawo la moyo
wako pa ntchito yako yolemetsa pansi pano. 10 Ntchito iliyonse imene
ukuyigwira, uyigwire ndi mphamvu zako zonse, pakuti ku manda kumene
ukupita kulibe kugwira ntchito, kulibe malingaliro, chidziwitso ndiponso
nzeru.
11 Ine ndinaonanso chinthu china pansi pano:
opambana pa kuthamanga si aliwiro,
kapena opambana pa nkhondo si amphamvu,
ndiponso okhala ndi chakudya si anzeru,
kapena okhala ndi chuma si odziwa zambiri,
kapena okomeredwa mtima si ophunzira;
koma mwayi umangowagwera onsewa pa nthawi yake.
12 Kungoti palibe munthu amene amadziwa kuti nthawi yake idzafika
liti:
monga momwe nsomba zimagwidwira mu ukonde,
kapena mmene mbalame zimakodwera mu msampha,
chimodzimodzinso anthu amakodwa mu msampha pa nthawi yoyipa,
pamene tsoka limawagwera mosayembekezera.

### *Nzeru Iposa Uchitsiru*

13 Ine ndinaonanso pansi pano chitsanzo ichi cha nzeru chimene
chinandikhudza kwambiri: 14 Panali mzinda waung'ono umene unali ndi
anthu owerengeka. Ndipo mfumu yamphamvu inabwera kudzawuthira
nkhondo, inawuzungulira ndi kumanga mitumbira yankhondo. 15 Tsono
mu mzindamo munali munthu wosauka koma wanzeru, ndipo anapulu-
mutsa mzindawo ndi nzeru zakezo. Koma palibe amene anakumbukira
munthu wosaukayo. 16 Choncho ine ndinati, "Nzeru ndi yopambana
mphamvu." Koma nzeru ya munthu wosauka imanyozedwa, ndipo palibe
amene amalabadirako za mawu ake.
17 Mawu oyankhula mofatsa a munthu wanzeru, anthu amawasamalira kwambiri
kupambana kufuwula kwa mfumu ya zitsiru.
18 Nzeru ndi yabwino kupambana zida zankhondo,
koma wochimwa mmodzi amawononga zinthu zambiri zabwino.

## 10

1 Monga ntchentche zakufa zimayika fungo loyipa m'mafuta onunkhira,
choncho kupusa pang'ono kumawononganso nzeru ndi ulemu.

2 Mtima wa munthu wanzeru umamutsogolera bwino,
koma mtima wa munthu wopusa umamusocheretsa.
3 Chitsiru ngakhale chikamayenda mu msewu,
zochita zake ndi zopanda nzeru
ndipo chimaonetsa aliyense kuti icho ndi chitsirudi.
4 Ngati wolamulira akukwiyira,
usachoke pa ntchito yako;
kufatsa kumakonza zolakwa zazikulu.

5 Pali choyipa chimene ndinachiona pansi pano,
kulakwitsa kumene kumachokera kwa wolamulira:
6 Zitsiru amazipatsa ntchito zambiri zapamwamba,
pamene anthu olemera amawapatsa ntchito zotsika.
7 Ndaona akapolo atakwera pa akavalo,
pamene akalonga akuyenda pansi ngati akapolo.

8 Amene amakumba dzenje adzagwamo yekha;
amene amabowola khoma adzalumidwa ndi njoka.
9 Amene amaphwanya miyala adzapwetekedwa ndi miyalayo;
amene amawaza nkhuni adzapwetekedwa nazo.

10 Ngati nkhwangwa ili yobuntha
yosanoledwa,
pamafunika mphamvu zambiri potema,
koma luso limabweretsa chipambano.

11 N’kopanda phindu kudziwa kuseweretsa njoka
ngati njokayo yakuluma kale.

12 Mawu a pakamwa pa munthu wanzeru ndi okondweretsa,
koma chitsiru chidzawonongedwa ndi milomo yake yomwe.
13 Chitsiru chimayamba ndi mawu opusa;
potsiriza pake zoyankhula zake ndi zamisala
14 ndipo chitsiru chimachulukitsa mawu.

Palibe amene amadziwa zimene zikubwera m’tsogolo,
ndani angamuwuze zomwe zidzachitika iye akadzafa?

15 Chitsiru chimatopa msanga ndi ntchito yochepa;
ndipo sichikhala ndi mphamvu zobwererera ku mudzi.

16 Tsoka kwa iwe, iwe dziko ngati mfumu yako ikali mwana,
ndipo atsogoleri ako amakhala pa madyerero mmamawa.
17 Wodala iwe, iwe dziko ngati mfumu yako ndi mwana wolemekezeka
ndipo atsogoleri ako amadya pa nthawi yake,
kuti apeze mphamvu osati kuti aledzere.

18 Ngati munthu ndi waulesi, denga lake limaloshoka;
ngati manja ake ndi alobodo nyumba yake imadontha.

19 Phwando ndi lokondweretsa anthu,
ndipo vinyo ndi wosangalatsa moyo,

koma ndalama ndi yankho la chilichonse.

20 Usanyoze mfumu ngakhale mu mtima mwako,
kapena kutukwana munthu wachuma m'chipinda chako,
pakuti mbalame yamlengalenga itha kutenga mawu ako
n'kukafotokoza zomwe wanena.

# 11

*Kuponya Chakudya pa Madzi*

1 Ponya chakudya chako pa madzi,
udzachipezanso patapita masiku ambiri.
2 Ndalama zako uzisungitse kwa anthu asanu ndi awiri, inde kwa anthu asanu ndi atatu,
pakuti sudziwa ndi tsoka lanji limene likubwera pa dziko.

3 Ngati mitambo yadzaza ndi madzi,
imagwetsa mvula pa dziko lapansi.
Mtengo ukagwera cha kummwera kapena cha kumpoto,
ndiye kuti udzagonera kumene wagwerako.
4 Amene amayang'ana mphepo sadzadzala;
amene amayang'ana mitambo sadzakolola.

5 Momwe sudziwira mayendedwe a mphepo,
kapena momwe mzimu umalowera m'thupi la mwana m'mimba mwa amayi,
momwemonso sungathe kudziwa ntchito za Mulungu,
Mlengi wa zinthu zonse.

6 Dzala mbewu zako mmawa
ndipo madzulo usamangoti manja lobodo,
pakuti sudziwa chimene chidzapindula,
mwina ichi kapena icho,
kapena mwina zonse ziwiri zidzachita bwino.

*Kumbukira Mlengi Wako*

7 Kuwala n'kwabwino,
ndipo maso amasangalala kuona dzuwa.
8 Munthu akakhala wa zaka zambiri,
mulekeni akondwerere zaka zonsezo,
koma iye azikumbukira masiku a mdima,
pakuti adzakhala ochuluka.
Chilichonse chimene chikubwera ndi chopanda phindu.

9 Kondwera mnyamata iwe, pamene ukanali wamng'ono,
ndipo mtima wako usangalale pa nthawi ya unyamata wako.
Tsatira zimene mtima wako ukufuna,
ndiponso zimene maso ako akuona,
koma dziwa kuti pa zinthu zonsezo
Mulungu adzakuweruza.
10 Choncho uchotse zokusautsa mu mtima mwako,
upewe zokupweteka m'thupi mwako,
pakuti unyamata ndi ubwana ndi zopandapake.

# 12

1 Uzikumbukira mlengi wako
masiku a unyamata wako,
masiku oyipa asanafike,
nthawi isanafike pamene udzanena kuti,
"Izi sizikundikondweretsa."
2 Nthawi ya ukalamba wako, dzuwa ndi kuwala,
mwezi ndi nyenyezi zidzada.
Mitambo idzabweranso mvula itagwa.
3 Nthawi imene manja ako adzanjenjemera,
miyendo yako idzafowoka,
pamene mano ako adzalephera kutafuna chifukwa ndi owerengeka,
ndipo maso ako adzayamba kuchita chidima.
4 Makutu ako adzatsekeka,
ndipo sudzamva phokoso lakunja;
sudzamvanso kusinja kwa pa mtondo
kapena kulira kwa mbalame mmawa.
5 Imeneyi ndiyo nthawi imene anthu amaopa kupita kumalo okwera,
amaopa kuyenda m'misewu;
Mutu umatuwa kuti mbuu,
amayenda modzikoka ngati ziwala
ndipo chilakolako chimatheratu.
Nthawi imeneyo munthu amapita ku nyumba yake yamuyaya
ndipo anthu olira maliro amayendayenda m'misewu.

6 Kumbukira Iye chingwe cha siliva chisanaduke,
kapena mbale yagolide isanasweke;
mtsuko usanasweke ku kasupe,
kapena mkombero usanathyoke ku chitsime.
7 Iyi ndi nthawi imene thupi lidzabwerera ku dothi, kumene linachokera,
mzimu udzabwerera kwa Mulungu amene anawupereka.

8 "Zopanda phindu! Zopandapake!" akutero Mlaliki.
"Zonse ndi zopandapake!"

### *Mawu Otsiriza*

9 Mlaliki sanali wozindikira zinthu kokha ayi, komanso ankaphunzitsa
anthu. Iye ankasinkhasinkha ndi kufufuzafufuza ndi kulemba mwadon-
gosolo miyambi yambiri. 10 Mlaliki anafufuzafufuza kuti apeze mawu
oyenera, ndipo zimene analemba zinali zolondola ndiponso zoona.
11 Mawu a anthu anzeru ali ngati zisonga, zokamba zawo zimene
anasonkhanitsa zili ngati misomali yokhomera, yoperekedwa ndi m'busa
mmodzi. 12 Samalira mwana wanga, za kuwonjezera chilichonse pa
zimenezi.

Kulemba mabuku ambiri sikutha, ndipo kuphunzira kwambiri kumatopetsa thupi.

13 Basi zonse zamveka; mathero a nkhaniyi ndi awa:
uziopa Mulungu ndi kusunga malamulo ake,
pakuti umenewu ndiwo udindo
wa anthu onse.
14 Pakuti Mulungu adzaweruza zochita zonse,
kuphatikizanso zinthu zonse zobisika,
kaya zabwino kapena zoyipa.

# Nyimbo ya Solomoni

1 Nyimbo ya Solomoni, nyimbo yoposa nyimbo zonse.

*Mkazi*
2 Undipsompsone ndi milomo yako
chifukwa chikondi chako n'chokoma kuposa vinyo.
3 Mafuta ako odzola ndi onunkhira bwino;
dzina lako lili ngati mafuta onunkhira otsanulidwa.
N'chifukwa chake atsikana amakukonda!
4 Nditenge ndipo ndizikutsata, tiye tifulumire!
Mfumu indilowetse m'chipinda chake.
*Abwenzi*
Ife timasangalala ndi kukondwera nawe,
tidzatamanda chikondi chako kupambana vinyo.
*Mkazi*
Amachita bwinotu potamanda iwe!

5 Ndine wakuda, komatu ndine wokongola,
inu akazi a ku Yerusalemu,
ine ndine wakuda ngati tenti ya ku Kedara,
ngati makatani a tenti ya Solomoni.
6 Musandiyang'ane monyoza chifukwa ndine wakuda,
ndine wakuda chifukwa cha dzuwa.
Alongo anga anandikwiyira
ndipo anandigwiritsa ntchito m'minda ya mpesa;
munda wangawanga sindinawusamalire.
7 Ndiwuze iwe, amene ndimakukonda, kumene umadyetsa ziweto zako
ndi kumene umagoneka nkhosa zako nthawi yamasana.
Ndikhalirenji ngati mkazi wachiwerewere
pambali pa ziweto za abwenzi ako?
*Abwenzi*
8 Ngati sukudziwa iwe wokongola kwambiri kuposa akazi ena,
ngati sukudziwa, tsatira makwalala a nkhosa
ndipo udyetse ana ambuzi
pambali pa matenti a abusa.
*Mwamuna*
9 Iwe bwenzi langa,
uli ngati kavalo wamkazi ku magaleta a Farao.
10 Masaya ako ndi okongola ndi ndolo zam'makutuzo,
khosi lako likukongola ndi mikanda yamiyala yamtengowapatali.
11 Tidzakupangira ndolo zagolide
zokongoletsedwa ndi mikanda yasiliva.
*Mkazi*
12 Pamene mfumu inali pa malo ake odyera,
mafuta anga onunkhira anamveka fungo lake.
13 Wokondedwa wanga ali ngati kathumba ka mure kwa ine,
kamene kamakhala pakati pa mawere angawa.
14 Wokondedwa wanga ali ngati mpukutu wa maluwa ofiira,

ochokera ku minda ya mpesa ya ku Eni-Gedi.
*Mwamuna*
15 Iwe wokondedwa wanga, ndiwe wokongoladi!
Ndithu, ndiwe chiphadzuwa,
maso ako ali ngati nkhunda.
*Mkazi*
16 Iwe bwenzi langa, ndiwe wokongoladi!
Ndithu, ndiwe wokongoladi kwambiri!
Ndipo malo athu ogonapo ndi msipu wobiriwira.
*Mwamuna*
17 Mitanda ya nyumba yathu ndi ya mkungudza,
phaso lake ndi la mtengo wa payini.

# 2

*Mkazi*
1 Ine ndine duwa la ku Saroni,
duwa lokongola la ku zigwa.
*Mwamuna*
2 Monga duwa lokongola pakati pa minga
ndi momwe alili wokondedwa wanga pakati pa atsikana.
*Mkazi*
3 Monga mtengo wa apulosi pakati pa mitengo ya m'nkhalango
ndi momwe alili bwenzi langa pakati pa anyamata.
Ndimakondwera kukhala pansi pa mthunzi wako,
ndipo chipatso chake ndi chokoma m'kamwa mwanga.
4 Iye wanditengera ku nyumba yaphwando,
ndipo mbendera yake yozika pa ine ndi chikondi.
5 Undidyetse keke ya mphesa zowuma,
unditsitsimutse ndi ma apulosi,
pakuti chikondi chandifowoketsa.
6 Mutu wanga watsamira dzanja lake lamanzere,
ndipo dzanja lake lamanja landikumbatira.
7 Inu akazi a ku Yerusalemu, ndithu ndikukupemphani
pali gwape ndi mbawala yayikazi zakuthengo:
Musachigwedeze chikondi kapena kuchiutsa
mpaka pamene chifunire ichocho.

8 Tamverani bwenzi langa!
Taonani! Uyu akubwera apayu,
akulumphalumpha pa mapiri,
akujowajowa pa zitunda.
9 Bwenzi langa ali ngati gwape kapena mwana wa mbawala.
Taonani! Uyo wayima kuseri kwa khoma lathulo,
akusuzumira m'mazenera,
akuyang'ana pa mpata wa zenera.
10 Bwenzi langa anayankha ndipo anati kwa ine,
"Dzuka bwenzi langa,
wokongola wanga, ndipo tiye tizipita.
11 Ona, nyengo yozizira yatha;
mvula yatha ndipo yapitiratu.
12 Maluwa ayamba kuoneka pa dziko lapansi;
nthawi yoyimba yafika,
kulira kwa njiwa kukumveka

m'dziko lathu.
13 Mtengo wankhuyu ukubereka zipatso zake zoyambirira;
mitengo ya mpesa ya maluwa ikutulutsa fungo lake.
Dzuka bwenzi langa, wokongola wanga
tiye tizipita."

*Mwamuna*

14 Nkhunda yanga yokhala m'ming'alu ya thanthwe,
m'malo obisala a m'mbali mwa phiri,
onetsa nkhope yako,
n'tamvako liwu lako;
pakuti liwu lako ndi lokoma,
ndipo nkhope yako ndi yokongola.
15 Mutigwirire nkhandwe,
nkhandwe zing'onozing'ono
zimene zikuwononga minda ya mpesa,
minda yathu ya mpesa imene yayamba maluwa.

*Mkazi*

16 Bwenzi langa ndi wangadi ndipo ine ndine wake;
amadyetsa gulu lake la ziweto pakati pa maluwa okongola.
17 Kamphepo kamadzulo kakayamba kuwuzira
ndipo mithunzi ikayamba kuthawa,
unyamuke bwenzi langa,
ndipo ukhale ngati gwape
kapena ngati mwana wa mbawala
pakati pa mapiri azigwembezigwembe.

## 3

1 Usiku wonse ndili pa bedi langa
ndinafunafuna amene mtima wanga umamukonda;
ndinamufunafuna koma osamupeza.
2 Ndikudzuka tsopano ndipo ndidzayendayenda mu mzinda,
m'misewu yake ndi m'mabwalo ake;
ndidzamufunafuna amene mtima wanga umamukonda.
Kotero ine ndinamufunafuna iyeyo koma osamupeza.
3 Alonda anandipeza
pamene ankayendera mzinda.
"Kodi mwamuonako amene mtima wanga umamukonda?"
4 Nditawapitirira pang'ono
ndinamupeza amene mtima wanga umamukonda.
Ndinamugwira ndipo sindinamulole kuti achoke
mpaka nditamulowetsa m'nyumba ya amayi anga,
m'chipinda cha amene anandibereka.
5 Inu akazi a ku Yerusalemu, ndithu ndikukupemphani
pali gwape ndi mbawala yayikazi zakuthengo:
Musachigwedeze chikondi kapena kuchiutsa
mpaka pamene chifunire ichocho.

6 Kodi ndani amene akubwera kuchokera ku chipululu
ngati utsi watolotolo,
wonunkhira mure ndi lubani,
zopangidwa kuchokera ku zonunkhira zonse za anthu amalonda?
7 Ona! Chimenecho ndi chonyamulira Solomoni,

choperekezedwa ndi asilikali 60,
anthu amphamvu a ku Israeli,
8 onse atanyamula lupanga,
onse odziwa bwino nkhondo,
aliyense ali ndi lupanga pambali pake,
kukonzekera zoopsa za usiku.
9 Mfumu Solomoni anadzipangira chonyamulirachi;
anachipanga ndi matabwa ochokera ku Lebanoni.
10 Milongoti yake anayipanga yasiliva,
kumbuyo kwake kwa golide.
Mipando yake inakutidwa ndi nsalu yapepo,
anakongoletsa m'kati mwake ndi chikondi
cha akazi a ku Yerusalemu.
11 Tukulani inu akazi a ku Ziyoni
ndipo mudzaone mfumu Solomoni atavala chipewa chaufumu,
chipewa chaufumu chimene amayi ake anamuveka
pa tsiku la ukwati wake,
tsiku limene mtima wake unasangalala.

# 4

*Mwamuna*

1 Ndiwe wokongoladi wokondedwa wanga!
Ndithudi, ndiwe wokongola!
Maso ako ali ngati nkhunda kumbuyo kwa nsalu yophimba kumutu.
Tsitsi lako lili ngati gulu la mbuzi
zikutsetsereka kuchokera ku Giliyadi.
2 Mano ako ali ngati gulu la nkhosa zomwe zangometedwa kumene,
zochokera kozisambitsa kumene.
Iliyonse ili ndi ana amapasa;
palibe imene ili yokha.
3 Milomo yako ili ngati mbota yofiira;
pakamwa pako ndi pokongola kwambiri.
Kukhalira kumbuyo kwa nsalu yako yophimba
kumutuyo, masaya ako akuoneka ngati mabandu a makangadza.
4 Khosi lako lili ngati nsanja ya Davide,
yomangidwa bwino ndi yosalala;
pa nsanja imeneyo pali zishango 1,000,
zishango zonsezo za anthu ankhondo.
5 Mawere ako ali ngati tiana tiwiri ta nswala,
ngati ana amapasa a nswala
amene akudya pakati pa maluwa okongola.
6 Kamphepo kamadzulo kakayamba kuwuzira
ndipo mithunzi ikayamba kuthawa,
ndidzapita ku phiri la mure
ndi ku chitunda cha lubani.
7 Ndiwe wokongola kwambiri wokondedwa wanga;
palibe chilema pa iwe.

8 Tiye tichoke ku Lebanoni iwe mkwatibwi wanga,
tiye tichoke ku Lebanoni,
utsikepo pa msonga ya Amana,
kuchoka pa msonga ya phiri la Seniri, pamwamba penipeni pa Herimoni,

kuchoka ku mapanga a mikango
ndiponso kumapiri kumene akambuku amavutitsa.
9 Iwe mlongo wanga, mkwatibwi wanga, wanditenga mtima,
iwe wanditenga mtima
ndi kapenyedwe ka maso ako,
ndiponso ndi umodzi mwa mikanda ya m'khosi mwako.
10 Iwe mlongo wanga, mkwatibwi wanga, chikondi chako n'chosangalatsa!
Chikondi chako n'chosangalatsa kwambiri kupambana vinyo,
ndiponso fungo la mafuta ako ndi lopambana zonunkhiritsa zonse!
11 Iwe mkwatibwi wanga, milomo yako ikuchucha uchi ngati chisa cha njuchi;
pansi pa lilime lako pali mkaka ndi uchi.
Fungo lonunkhira la zovala zako likumveka ngati fungo la ku Lebanoni.
12 Iwe mlongo wanga, mkwatibwi wanga, ndiwe munda wopiringidzidwa;
ndiwe kasupe wotchingidwa, chitsime chotetezedwa.
13 Zomera zako ndi munda wa zipatso za makangadza;
muli zipatso zokoma kwambiri,
muli hena ndi nadi,
14 nadi ndi safiro,
kalamusi ndi sinamoni,
komanso mtengo uliwonse wonunkhira bwino.
Mulinso mure ndi aloe
ndi zonunkhiritsa zonse zabwino kwambiri.
15 Iwe ndiwe kasupe wa m'munda,
chitsime cha madzi oyenda,
mtsinje wa madzi ochokera ku Lebanoni.

*Mkazi*

16 Dzuka, iwe mphepo yakumpoto,
ndipo bwera, iwe mphepo yakummwera!
Uzira pa munda wanga,
kuti fungo lake lonunkhira lifalikire ponseponse.
Bwenzi langa alowe m'munda mwake
ndi kudya zipatso zake zabwino kwambiri.

# 5

*Mwamuna*

1 Ndalowa m'munda mwanga, iwe mlongo wanga, iwe mkwatibwi wanga;
ndasonkhanitsa mure wanga ndi zokometsera zakudya zanga.
Ndadya uchi wanga pamodzi ndi zisa zake zomwe;
ndamwa vinyo wanga ndi mkaka wanga.

*Abwenzi*

Idyani abwenzi anga, imwani;
Inu okondana, imwani kwambiri.

*Mkazi*

2 Ndinagona tulo koma mtima wanga unali maso.
Tamverani, bwenzi langa akugogoda:
"Nditsekulire, mlongo wanga, bwenzi langa,
nkhunda yanga, wangwiro wanga.
Mutu wanga wanyowa ndi mame,
tsitsi langa lanyowa chifukwa cha nkhungu ya usiku."
3 Ndavula kale zovala zanga,
kodi ndizivalenso?

Ndasamba kale mapazi anga
kodi ndiwadetsenso?
4 Bwenzi langa anapisa dzanja lake pa chibowo cha pa chitseko;
mtima wanga unagunda chifukwa cha iye.
5 Ndinanyamuka kukamutsekulira wachikondi wangayo,
ndipo manja anga anali noninoni ndi mure,
zala zanga zinali mure chuchuchu,
pa zogwirira za chotsekera.
6 Ndinamutsekulira wachikondi wanga,
koma n'kuti wachikondi wangayo atachoka; iye anali atapita.
Mtima wanga unafumuka chifukwa cha kuchoka kwake.
Ndinamuyang'anayang'ana koma sindinamupeze.
Ndinamuyitana koma sanandiyankhe.
7 Alonda anandipeza
pamene ankayendera mzindawo.
Anandimenya ndipo anandipweteka;
iwo anandilanda mwinjiro wanga,
alonda a pa khoma aja!
8 Inu akazi a ku Yerusalemu ndithu ndikukupemphani,
mukapeza wokondedwa wangayo,
kodi mudzamuwuza chiyani?
Muwuzeni kuti ine ndadwala nacho chikondi.

*Abwenzi*

9 Iwe wokongola kuposa akazi onsewa,
kodi wokondedwa wakoyo ndi wopambana wina aliyense bwanji?
Kodi wokondedwa wakoyo ndi wopambana ena onse chotani
kuti uzichita kutipempha motere?

*Mkazi*

10 Wokondedwa wangayo ndi wowala kwambiri ndi wathanzi
pakati pa anthu 1,000.
11 Mutu wake ndi golide woyengeka bwino;
tsitsi lake ndi lopotanapotana,
ndiponso lakuda bwino ngati khwangwala.
12 Maso ake ali ngati nkhunda
m'mbali mwa mitsinje ya madzi,
ngati nkhunda zitasamba mu mkaka,
zitayima ngati miyala yamtengowapatali.
13 Masaya ake ali ngati timinda ta mbewu zokometsera zakudya
zopatsa fungo lokoma.
Milomo yake ili ngati maluwa okongola
amene akuchucha mure.
14 Manja ake ali ngati ndodo zagolide
zokongoletsedwa ndi miyala yamtengowapatali.
Thupi lake ndi losalala ngati mnyanga wanjovu
woyikamo miyala ya safiro.
15 Miyendo yake ili ngati mizati yamwala,
yokhazikika pa maziko a golide.
Maonekedwe ake ali ngati Lebanoni,
abwino kwambiri ngati mkungudza.
16 Milomo yake ndi yosangalatsa kwambiri;
munthuyo ndi wokongola kwambiri!
Uyu ndiye wachikondi wanga ndi bwenzi langa,
inu akazi a ku Yerusalemu.

# 6

*Abwenzi*
1 Iwe wokongola kuposa akazi onsewa,
kodi wokondedwa wakoyo wapita kuti?
Kodi wokondedwa wakoyo wakhotera njira iti
kuti timufunefune pamodzi ndi iwe?
*Mkazi*
2 Wachikondi wanga watsikira ku munda kwake,
ku timinda ta zokometsera zakudya,
akukadyetsa ziweto zake ku minda,
ndiponso akuthyola maluwa okongola.
3 Wokondedwa wangayo ndine wake ndipo iyeyo ndi wangawanga;
amadyetsa ziweto zake pakati pa maluwa okongola.
*Mwamuna*
4 Ndiwe wokongola, bwenzi langa, ngati Tiriza,
wokongola kwambiri ngati Yerusalemu,
ndiwe woopsa ngati gulu lankhondo lonyamula mbendera.
5 Usandipenyetsetse;
pakuti maso ako amanditenga mtima.
Tsitsi lako lili ngati gulu la mbuzi
zikutsetsereka kuchokera ku Giliyadi.
6 Mano ako ali ngati gulu la nkhosa
zimene zikubwera kuchokera kokazisambitsa,
iliyonse ili ndi ana amapasa,
palibe imene ili yokha.
7 Kukhalira kumbuyo kwa nsalu yako yophimba kumutu,
masaya ako ali ngati mabandu a makangadza.
8 Ngakhale patakhala akazi a mfumu 60,
ndi azikazi 80,
ndi anamwali osawerengeka;
9 koma nkhunda yanga, wangwiro wanga ndi wosiyana ndi wina aliyense;
mwana wamkazi yekhayo wa amayi ake,
mwana wapamtima wa amene anamubereka.
Anamwali anamuona ndipo anamutcha wodala;
akazi a mfumu ndi azikazi anamutamanda.
*Abwenzi*
10 Ndani uyu akuoneka ngati m'bandakucha,
wokongola ngati mwezi, wowala ngati dzuwa,
wochititsa mantha ngati gulu la ankhondo mbendera zili m'manja?
*Mwamuna*
11 Ndinatsikira ku munda wa mitengo ya alimondi
kukayang'ana zomera zatsopano ku chigwa,
kukaona ngati mpesa waphukira
kapena ngati makangadza ali ndi maluwa.
12 Ndisanazindikire kanthu,
ndinakhala ngati ndikulota kuti ndili m'galeta pambali pa mfumu yanga.
*Abwenzi*
13 Bwerera, bwerera iwe namwali wa ku Sulami;
bwerera, bwerera kuti ife tidzakupenyetsetse iwe!
*Mwamuna*
Chifukwa chiyani mukufuna kudzapenyetsetsa ine mwana wamkazi wa ku Sulami,

pamene ndikuvina pakati pa magulu awiri?

# 7

1 Iwe namwali waufumu, mapazi ako ngokongola
mu nsapato wavalazo!
Ntchafu zako n'zowumbika bwino ngati miyala yamtengowapatali,
ntchito ya manja ya mmisiri waluso.
2 Mchombo wako uli ngati chikho chowumbika bwino
chimene nthawi zonse ndi chodzaza ndi vinyo.
Chiwuno chako ndi choning'a ngati mtolo wa tirigu
utazunguliridwa ndi maluwa okongola.
3 Mawere ako akuoneka ngati ana awiri a mbawala,
ngati mphoyo zamapasa.
4 Khosi lako lili see! ngati nsanja ya mnyanga wa njovu.
Maso ako ali ngati mayiwe a ku Hesiboni,
amene ali pafupi ndi chipata cha Bati Rabimu.
Mphuno yako ili ngati nsanja ya ku Lebanoni,
yoyang'ana ku Damasiko.
5 Mutu wako uli bwinobwino neng'aa ngati phiri la Karimeli.
Tsitsi lako lili ngati nsalu yakuda yaufumu;
mfumu yakopeka ndi maonekedwe ake okongola.
6 Ndiwe wokongola kwambiri ndiponso wosangalatsa,
iwe wokondedwa, namwali wokondweretsawe!
7 Msinkhu wako uli ngati mtengo wa mgwalangwa,
ndipo mawere ako ali ngati phava la zipatso.
8 Ndinati, "Ndikwera mtengo wa mgwalangwa;
ndidzathyola zipatso zake."
Mawere ako ali ngati maphava a mphesa,
fungo la mpweya wako lili ngati ma apulosi,
9 ndipo pakamwa pako pali ngati vinyo wokoma kwambiri.

*Mkazi*

Tsono vinyo ameneyu amuthirire wachikondi wanga,
ayenderere bwino pa milomo yake ndi mano ake.
10 Wokondedwayo ine ndine wake,
ndipo chilakolako chake chili pa ine.
11 Bwera wachikondi wanga, tiye tipite ku madera a ku midzi,
tikagone ku midzi.
12 Tiye tilawirire mmamawa kupita ku minda ya mpesa,
tikaone ngati mitengo ya mpesa yayamba kuphukira,
ngati maluwa ake ayamba kuoneka,
komanso ngati makangadza ayamba kuonetsa maluwa.
Kumeneko ndidzakuonetsa chikondi changa.
13 Mitengo ya mankhwala a chisulo ikupereka fungo lake labwino,
ndipo pa khomo pathu pali zipatso zonse zokoma,
zatsopano ndi zakale zomwe,
zimene ndakusungira wokondedwa wanga.

# 8

1 Ukanakhala kuti ndiwe mlongo wanga,
amene anayamwa mawere a amayi anga!
Ndikanakumana nawe pa njira,
ndikanakupsompsona,

ndipo palibe wina aliyense akanandinyoza.
2 Ndikanakutenga
ndi kukulowetsa m'nyumba ya amayi anga,
amayi amene anandiphunzitsa,
ndikanakupatsa vinyo wotsekemera kuti umwe,
zotsekemera za makangadza.
3 Mutu wanga watsamira dzanja lake lamanzere
ndipo dzanja lake lamanja landikumbatira.
4 Inu akazi a ku Yerusalemu, ndithu ndikukupemphani:
musachigwedeze chikondi kapena kuchiutsa
mpaka pamene chifunire ichocho.

*Abwenzi*

5 Kodi ndani uyo akutuluka ku chipululuyo,
atatsamira wokondedwa wakeyo?

*Mkazi*

Ndinakudzutsa pa tsinde pa mtengo wa apulosi,
pamenepo ndi pamene amayi anachirira,
pamenepo ndi pamene wokubereka anamva ululu pokubala iweyo.
6 Undiyike pamtima pako ngati chidindo,
ngati chidindo cha pa dzanja lako;
pakuti chikondi n'champhamvu ngati imfa,
nsanje ndiyaliwuma ngati manda.
Chikondi chimachita kuti lawilawi
ngati malawi a moto wamphamvu.
7 Madzi ochuluka sangachizimitse chikondi,
mitsinje singachikokolole chikondicho.
Ngati wina apereka chuma chonse
cha m'nyumba mwake chifukwa cha chikondi,
adzangonyozeka nazo kotheratu.

*Abwenzi*

8 Ife tili naye mlongo wathu wamng'ono,
koma alibe mawere,
kodi tidzamuchitira chiyani mlongo wathuyu
pa tsiku limene adzamufunsire?
9 Ngati iye ndi khoma,
tidzamumangira nsanja ya siliva.
Ngati iye ndi chitseko,
tidzamutchinga ndi matabwa a mkungudza.

*Mkazi*

10 Ine ndili ngati khoma,
ndipo mawere anga ndi nsanja zake.
Tsono m'maso mwa bwenzi langa
ndine wobweretsa mtendere.
11 Solomoni anali ndi munda wampesa ku Baala-Hamoni;
iyeyo anabwereketsa munda wamphesawo kwa alimi,
aliyense mwa iwo ankayenera kupereka
ndalama zasiliva 1,000 m'malo mwa zipatso zake.
12 Koma munda wanga wampesa ndi wangawanga ndiponso wa ine ndekha.
Iwe Solomoni, khala nazo ndalama zasiliva 1,000
ndipo ndalama zasiliva 200 ndi za amene akusamalira mundawo.

*Mwamuna*

13 Iwe amene umakhala m'minda

uli pamodzi ndi anzako,
ndilole kuti ndimve liwu lako!

*Mkazi*

14 Fulumira wokondedwa wanga,
ndipo ukhale ngati gwape
kapena mwana wa mbawala
wothamanga m'mapiri m'mene mumamera mbewu zokometsera chakudya.

# Yesaya

1 Masomphenya wonena za Yuda ndi Yerusalemu, amene Yesaya mwana
wa Amozi, anaona pa nthawi ya ulamuliro wa Uziya, Yotamu, Ahazi ndi
Hezekiya, mafumu a Yuda.

*Anthu Owukira*

2 Tamverani, miyamba inu! Tchera khutu, iwe dziko lapansi!
Pakuti Yehova wanena kuti,
“Ndinabala ana ndi kuwalera,
koma anawo andiwukira Ine.
3 Ng’ombe imadziwa mwini wake,
bulu amadziwa kumene kuli gome la mbuye wake,
koma Israeli sadziwa,
anthu anga samvetsa konse.”

4 Haa, mtundu wochimwa,
anthu olemedwa ndi machimo,
obadwa kwa anthu ochita zoyipa,
ana odzipereka ku zoyipa!
Iwo asiya Yehova;
anyoza Woyerayo wa Israeli
ndipo afulatira Iyeyo.

5 Chifukwa chiyani mukufuna kuti muzingolangidwabe?
Chifukwa chiyani mukupitirira kukhala m’moyo wowukira?
Mutu wanu wonse uli ndi mabala,
mtima wanu wonse wafowokeratu.
6 Kuchokera ku phazi mpaka ku mutu
palibe pabwino,
paliponse pali mikwingwirima ndi zilonda,
mabala ali magazi chuchuchu,
mabala ake ngosatsuka, ngosamanga
ndiponso ngosapaka mafuta ofewetsa.

7 Dziko lanu lasanduka bwinja,
mizinda yanu yatenthedwa ndi moto;
minda yanu ikukololedwa ndi alendo
inu muli pomwepo,
dziko lanu lasanduka bwinja monga ngati lagonjetsedwa ndi alendo.
8 Mwana wamkazi wa Ziyoni watsala yekha
ngati nsanja m’munda wampesa,
ngati chisimba m’munda wa minkhaka,
ngati mzinda wozingidwa ndi nkhondo.
9 Yehova Wamphamvuzonse akanapanda
kutisiyira opulumuka,
tikanawonongeka ngati Sodomu,
tikanakhala ngati anthu a ku Gomora.

10 Imvani mawu a Yehova,
inu olamulira Sodomu;

mverani lamulo la Mulungu wathu,
inu anthu a ku Gomora!
11 Yehova akuti, “Kodi ndili nazo chiyani
nsembe zanu zochuluka?”
“Zandikola nsembe zanu zopsereza
za nkhosa zazimuna ndiponso mafuta a nyama zonenepa;
sindikusangalatsidwanso
ndi magazi ang’ombe zamphongo ndi a ana ankhosa ndi ambuzi zazimuna.
12 Ndani anakulamulirani kuti
mubwere nazo pamaso panga?
Ndani anakuwuzani kuti muzipondaponda m’mabwalo a nyumba yanga?
13 Siyani kubweretsa nsembe zachabechabezo!
Nsembe zanu zofukiza zimandinyansa Ine.
Sindingapirire misonkhano yanu yoyipa,
kapenanso zikondwerero za Mwezi Watsopano ndi Masabata.
14 Zikondwerero zanu za Mwezi Watsopano ndi masiku anu opatulika
ndimadana nazo.
Zasanduka katundu wondilemera;
ndatopa kuzinyamula.
15 Mukamatambasula manja anu popemphera,
Ine sindidzakuyang’anani;
ngakhale muchulukitse mapemphero anu,
sindidzakumverani.
Manja anu ndi odzaza ndi magazi;
16 sambani, dziyeretseni.
Chotsani pamaso panu
ntchito zanu zoyipa!
Lekani kuchita zoyipa,
17 phunzirani kuchita zabwino!
Funafunani chilungamo,
thandizani oponderezedwa.
Tetezani ana amasiye,
muwayimirire akazi amasiye pa milandu yawo.”

18 Yehova akuti,
“Tiyeni tsono tikambe mlandu wanu.
Ngakhale machimo anu ali ofiira,
adzayera ngati thonje.
Ngakhale ali ofiira ngati kapezi,
adzayera ngati ubweya wankhosa.
19 Ngati muli okonzeka kundimvera
mudzadya zinthu zabwino za m’dziko;
20 koma mukakana ndi kuwukira
mudzaphedwa ndi lupanga.”
Pakuti Yehova wayankhula.

21 Taonani momwe mzinda wokhulupirika
wasandukira wadama!
Mzinda umene kale unali wodzaza ndi chiweruzo cholungama;
mu mzindamo munali chilungamo,
koma tsopano muli anthu opha anzawo!

22 Siliva wako wasanduka wachabechabe,
vinyo wako wabwino wasungunulidwa ndi madzi.
23 Atsogoleri ako ndi owukira,
anthu ogwirizana ndi mbala;
onse amakonda ziphuphu
ndipo amathamangira mphatso.
Iwo sateteza ana amasiye;
ndipo samvera madandawulo a akazi amasiye.
24 N'chifukwa chake Ambuye Yehova Wamphamvu,
Wamphamvuyo wa Israeli, akunena kuti,
"Haa, odana nane ndidzawatha,
ndipo ndidzawabwezera ndekha adani anga.
25 Ndidzatambasula dzanja langa kuti ndilimbane nawe;
ndidzasungunula machimo ako n'kuwachotsa,
monga mmene amachotsera dzimbiri ndi mankhwala.
26 Ndidzabwezeretsa oweruza ako ngati masiku amakedzana,
aphungu ako ndidzawabwezeretsa ngati poyamba paja.
Kenaka iweyo udzatchedwa
mzinda wolungama,
mzinda wokhulupirika."

27 Ziyoni adzawomboledwa mwa chiweruzo cholungama,
anthu ake olapadi adzapulumutsidwa mwachilungamo.
28 Koma owukira ndi ochimwa adzawawonongera pamodzi,
ndipo amene asiya Yehova adzatheratu.

29 "Mudzachita nayo manyazi mitengo ya thundu
imene inkakusangalatsani;
mudzagwetsa nkhope chifukwa cha minda
imene munayipatula.
30 Mudzakhala ngati mtengo wa thundu umene masamba ake akufota,
mudzakhala ngati munda wopanda madzi.
31 Munthu wamphamvu adzasanduka ngati udzu wowuma,
ndipo ntchito zake zidzakhala ngati mbaliwali;
motero zonse zidzayakira limodzi,
popanda woti azimitse motowo."

# 2

### *Phiri la Yehova*

1 Nazi zinthu zokhudza Yuda ndi Yerusalemu, zimene Yesaya mwana wa
Amozi anaziona m'masomphenya:
2 M'masiku otsiriza,
phiri la Nyumba ya Yehova adzalikhazikitsa
kukhala lalitali kuposa mapiri ena onse,
lidzaonekera pamwamba pa mapiri ena onse,
ndipo mayiko onse adzathamangira kumeneko.
3 Anthu ambiri adzabwera ndikunena kuti,
"Tiyeni tikwere ku phiri la Yehova,
ku nyumba ya Mulungu wa Yakobo.
Iye adzatiphunzitsa njira zake,
ndipo tidzayenda m'njira zakezo."
Malangizo adzachokera ku Ziyoni,

mawu a Yehova adzachokera ku Yerusalemu.
4 Iye adzaweruza pakati pa mayiko,
ndipo adzathetsa kusamvana pakati pa anthu ambiri.
Anthuwo adzasandutsa malupanga awo kukhala makasu
ndiponso mikondo yawo kukhala zomwetera.
Mtundu wina sudzatenganso lupanga kumenyana ndi mtundu wina,
kapena kuphunziranso za nkhondo.

5 Inu nyumba ya Yakobo, bwerani,
tiyeni tiyende m'kuwala kwa Yehova.

*Tsiku la Yehova*

6 Inu Yehova mwawakana anthu anu,
nyumba ya Yakobo.
Iwo adzaza ndi zamatsenga zochokera Kummawa;
amawombeza mawula ngati Afilisti,
ndipo amayanjana ndi anthu osapembedza Mulungu.
7 Dziko lawo ndi lodzaza ndi siliva ndi golide;
ndipo chuma chawo ndi chosatha.
Dziko lawo ndi lodzaza ndi akavalo;
ndipo magaleta awo ankhondo ngosawerengeka.
8 Dziko lawo ndi lodzaza ndi mafano;
iwo amapembedza ntchito ya manja awo,
amagwadira zomwe anapanga ndi zala zawo.
9 Tsono munthu aliyense adzachepetsedwa
ndi kutsitsidwa.
Inu Yehova musawakhululukire.

10 Lowani m'matanthwe,
bisalani m'maenje,
kuthawa kuopsa kwa Yehova
ndi ulemerero wa ufumu wake!
11 Kudzikuza kwa anthu kudzatha,
ndipo kudzitama kwa anthu kudzawonongedwa;
Yehova yekha ndiye adzapatsidwe ulemu pa tsiku limenelo.

12 Yehova Wamphamvuzonse wakonzeratu tsiku
limene adzatsitse onse onyada ndi odzitama,
ndipo adzagonjetsa
onse amphamvu,
13 tsiku la mikungudza yonse ya ku Lebanoni, yayitali ndi yoonekera patali,
ndiponso la mitengo yonse ya thundu ya ku Basani,
14 tsiku la mapiri onse ataliatali
ndiponso la zitunda zonse zazitali,
15 tsiku la nsanja zonse zazitali
ndiponso malinga onse olimba,
16 tsiku la sitima zapamadzi zonse za ku Tarisisi
ndiponso la mabwato onse okongola.
17 Kudzikuza kwa munthu kudzatha
ndipo kudzitama kwa anthu kudzawonongedwa,
Yehova yekha ndiye adzapatsidwe ulemu tsiku limenelo,
18 ndipo mafano onse adzatheratu.

19 Anthu adzathawira m'mapanga a matanthwe
ndi m'maenje a nthaka,
kuthawa mkwiyo wa Yehova,
ndiponso ulemerero wa ufumu wake,
pamene Iye adzuka kugwedeza dziko lapansi.
20 Tsiku limenelo anthu adzatayira
mfuko ndi mileme
mafano awo asiliva ndi mafano awo agolide,
amene anawapanga kuti aziwapembedza.
21 Adzathawira m'mapanga a matanthwe
ndiponso m'ming'alu ya nthaka
kuthawa mkwiyo wa Yehova
ndiponso ulemerero wa ufumu wake,
pamene Iye adzuka kugwedeza dziko lapansi.

22 Lekani kudalira munthu,
amene moyo wake sukhalira kutha.
Iye angathandize bwanji wina aliyense?

# 3

*Chiweruzo pa Yerusalemu ndi Yuda*

1 Taonani tsopano, Ambuye
Yehova Wamphamvuzonse,
ali pafupi kuchotsa mu Yerusalemu ndi mu Yuda
zinthu pamodzi ndi thandizo;
adzachotsa chakudya chonse ndi madzi onse,
2 anthu amphamvu ndi asilikali ankhondo,
oweruza ndi aneneri,
anthu olosera ndi akuluakulu,
3 atsogoleri a ankhondo makumi asanu ndi anthu olemekezeka,
aphungu ndi anthu amatsenga ndi akatswiri pa za kulosera.

4 Ndidzawayikira anyamata kuti akhale mafumu awo;
ana akhanda ndiwo adzawalamulire.
5 Anthu adzazunzana,
munthu ndi munthu mnzake, mnansi ndi mnansi wake.
Anthu wamba adzanyoza
akuluakulu.

6 Munthu adzagwira m'bale wake
m'nyumba ya abambo awo, ndipo adzati,
"Iwe uli nawo mwinjiro, ndiye ukhale mtsogoleri wathu;
lamulira malo opasuka ano!"
7 Koma tsiku limenelo m'bale wakeyo adzafuwula kuti,
"Ayi, mavuto oterewa ndilibe mankhwala ake.
Ndilibe chakudya kapena chovala m'nyumba mwanga;
musasankhe ine kukhala mtsogoleri wa anthu."

8 Yerusalemu akudzandira,
Yuda akugwa;
zokamba zawo ndi ntchito zawo n'zotsutsana ndi Yehova,
sakulabadira ulemerero wa Mulungu.

9 Maonekedwe a nkhope zawo amawatsutsa;
amaonetsera poyera tchimo lawo ngati Sodomu;
salibisa tchimo lawolo.
Tsoka kwa iwo
odziputira okha mavuto.

10 Nena kwa olungama kuti zonse zidzawayendera bwino,
pakuti adzakondwera ndi phindu la ntchito zawo.
11 Tsoka kwa anthu oyipa! Mavuto ali pa iwo!
Adzalandira malipiro a zimene manja awo anachita.

12 Achinyamata akupondereza anthu anga,
ndipo amene akuwalamulira ndi akazi.
Aa, anthu anga, atsogoleri anu akukusocheretsani;
akukuchotsani pa njira yanu.

13 Yehova wakhala pamalo pake m'bwalo la milandu;
wakonzeka kuti aweruze anthu ake.
14 Yehova akuwazenga milandu
akuluakulu ndi atsogoleri a anthu ake:
"Ndinu amene mwawononga munda wanga wa mpesa;
nyumba zanu zadzaza ndi zolanda kwa amphawi.
15 N'chifukwa chiyani inu mukupsinja anthu anga,
n'kudyera masuku pamutu amphawi?"
Akutero Ambuye Yehova Wamphamvuzonse.

16 Yehova akunena kuti,
"Akazi a ku Ziyoni ngodzikuza kwambiri,
akuyenda atakweza makosi awo,
akukopa amuna ndi maso awo
akuyenda monyang'ama
akuliza zigwinjiri za m'miyendo yawo
17 N'chifukwa chake Ambuye, adzatulutsa zipere pa mitu ya akazi a ku Ziyoniwo;
Yehova adzachititsa dazi mitu yawo."
18 Tsiku limenelo Ambuye adzawachotsera zodzikongoletsera zawo: za
m'miyendo, za ku mutu za m'khosi, 19 ndolo ndi zibangiri, nsalu zophimba
pa nkhope, 20 maduku, zigwinjiri za m'miyendo ndi malamba, mabotolo a
zonunkhira ndi zithumwa, 21 mphete ndi zipini, 22 zovala za pa mphwando,
zipewa ndi mwinjiro, zikwama, 23 magalasi oyang'anira, zovala zosalala,
nduwira ndiponso nsalu za m'mapewa.
24 M'malo mwa kununkhira azidzanunkha,
m'malo mwa lamba, adzavala chingwe;
m'malo mwa tsitsi lopesa bwino, adzakhala ndi dazi;
m'malo mwa zovala zabwino, adzavala chiguduli;
m'malo mwa kunyadira kukongola adzachita manyazi.
25 Iwe Yerusalemu anthu ako aamuna adzaphedwa ndi lupanga,
asilikali ako adzafera ku nkhondo.
26 Pa zipata za Ziyoni padzakhala kubuma ndi kulira;
Iweyo udzasakazidwa n'kukhala pansi, ukugubuduzika pa fumbi.

# 4

1 Tsiku limenelo akazi asanu ndi awiri
adzagwira mwamuna mmodzi,
n'kunena kuti, "Ife tizidya chakudya chathuchathu,
ndi kuvala zovala zathu;
inu mungotilola kuti tidziyitanidwa ndi dzina lanu.
Tichotseni manyazi aumbeta!"

*Nthambi ya Yehova*

2 Tsiku limenelo Nthambi ya Yehova idzakhala yokongola ndi yaule-
merero, ndipo chipatso cha m'dziko chidzakhala chonyaditsa ndi chop-
ereka ulemerero kwa onse opulumuka mu Israeli. 3 Iwo amene adzatsale
mu Ziyoni, amene adzatsalire mu Yerusalemu, adzatchedwa oyera, onse
amene mayina awo alembedwa pakati pa anthu amoyo okhala mu
Yerusalemu. 4 Ambuye adzasambitsa akazi a Ziyoni ndi kuchotsa zonyansa
zawo. Adzatsuka magazi amene anakhetsedwa mu Yerusalemu ndi
mzimu wachiweruzo ndiponso mzimu wamoto. 5 Tsono Yehova adzayika
mtambo wake pamwamba ponse pa phiri la Ziyoni, ndipo pa onse
amene asonkhana masana padzakhala mtambo wa utsi ndipo usiku
padzakhala malawi amoto. Pamwamba pa zonse padzakhala ulemerero
wa Yehova. 6 Ulemerero wake udzakhala mthunzi wothawiramo kutentha
kwa masana, udzakhala malo opeweramo mphepo ndi owusiramo mvula.

# 5

*Nyimbo ya Munda Wamphesa*

1 Ndidzamuyimbira bwenzi langa
nyimbo yokamba za munda wake wa mpesa:
Wokondedwa wanga anali ndi munda wamphesa
pa phiri la nthaka yachonde.
2 Anatipula nachotsa miyala yonse
ndipo anawokamo mipesa yabwino kwambiri.
Anamanga nsanja yolondera pakati pa mundawo
ndipo anasemanso mopsinyira mphesa m'mundamo.
Ndipo iye anayembekezera kuti mundawo udzabala mphesa zabwino,
koma ayi, unabala mphesa zosadya.

3 "Tsopano, inu amene mumakhala mu Yerusalemu ndi inu anthu a ku Yuda,
weruzani pakati pa ine ndi munda wanga wa mpesawu.
4 Kodi n'chiyaninso china chimene ndikanachitira munda wanga wa mpesa
kupambana chomwe ndawuchitira kale?
Pamene ndinkayembekezera kuti udzabala mphesa zabwino,
bwanji unabala mphesa zosadya?
5 Tsopano ndikuwuzani
chimene ndidzawuchitire munda wanga wa mpesa:
ndidzachotsa mpanda wake,
ndipo mundawo udzawonongeka;
ndidzagwetsa khoma lake,
ndipo nyama zidzapondapondamo.
6 Ndidzawusandutsa tsala,
udzakhala wosatengulira ndi wosalimira
ndipo mudzamera mkandankhuku ndi minga ina.

Ndidzalamula mitambo
kuti isagwetse mvula pa mundapo."

7 Munda wamphesa wa Yehova Wamphamvuzonse
ndi Aisraeli,
ndipo anthu a ku Yuda ndiwo
minda yake yomukondweretsa.
Ndipo Iye ankayembekezera chiweruzo cholungama, m'malo mwake anaona kuphana;
m'malo mwa chilungamo Iye anamva kulira kwa anthu ozunzika.

*Tsoka ndi Chiweruzo*

8 Tsoka kwa inu amene mumangokhalira kulumikiza nyumba,
ndipo mumangokhalira kuwonjezera minda,
mpaka mutalanda malo onse
kuti muzikhalamo nokha m'dzikomo.
9 Yehova Wamphamvuzonse wayankhula ine ndikumva kuti,
"Ndithudi nyumba zambirizo zidzasanduka mabwinja,
nyumba zazikulu zokongolazo zidzakhala zopanda anthu.
10 Munda wamphesa wa maekala khumi udzatulutsa vinyo wodzaza mbiya imodzi,
kufesa madengu khumi a mbewu, zokolola zake zidzangodzaza dengu limodzi."

11 Tsoka kwa iwo amene amadzuka mmamawa
nathamangira chakumwa choledzeretsa,
amene amamwa mpaka usiku
kufikira ataledzera kotheratu.
12 Pa maphwando awo pamakhala azeze, apangwe,
matambolini, zitoliro ndi vinyo,
ndipo sasamala ntchito za Yehova,
salemekeza ntchito za manja ake.
13 Motero anthu anga adzatengedwa ukapolo
chifukwa cha kusamvetsa zinthu;
atsogoleri awo olemekezeka adzafa ndi njala,
ndipo anthu wamba ochuluka adzafa ndi ludzu.
14 N'chifukwa chake ku manda sikukhuta
ndipo kwayasama kwambiri kukamwa kwake;
m'mandamo mudzagweranso anthu otchuka a mu Yerusalemu pamodzi ndi anthu wamba ochuluka;
adzagweramo ali wowowo, n'kuledzera kwawoko.
15 Ndipo munthu aliyense adzatsitsidwa,
anthu onse adzachepetsedwa,
anthu odzikuza adzachita manyazi.
16 Koma Yehova Wamphamvuzonse adzalemekezedwa chifukwa cha chiweruzo chake cholungama.
Ndipo Mulungu woyera adzadzionetsa kuti ndi woyera pochita chilungamo chake.
17 Tsono nkhosa zidzadya pamenepo ngati pabusa pawo;
ana ankhosa adzadya m'mabwinja a anthu olemera.

18 Tsoka kwa amene amadzikokera tchimo ndi zingwe zachinyengo,
ndipo amadzikokera zoyipa ndi zingwe zokokera ngolo,

19 amene amanena kuti, “Yehova afulumire,
agwire ntchito yake mwamsanga
kuti ntchitoyo tiyione.
Ntchito zionekere,
zimene Woyerayo wa Israeli akufuna kuchita,
zichitike kuti tizione.”

20 Tsoka kwa amene zoyipa amaziyesa zabwino
ndipo zabwino amaziyesa zoyipa,
amene mdima amawuyesa kuwala
ndipo kuwala amakuyesa mdima,
amene zowawasa amaziyesa zotsekemera
ndipo zotsekemera amaziyesa zowawasa.

21 Tsoka kwa amene amadziona ngati anzeru
ndipo amadziyesa ochenjera.

22 Tsoka kwa zidakwa zimene zimayika mtima pa vinyo
ndipo ndi akatswiri posakaniza zakumwa,
23 amene amamasula olakwa chifukwa cha chiphuphu
koma amayipitsa mlandu wa munthu wosalakwa.
24 N’chifukwa chake monga momwe moto umawonongera chiputu
ndipo monga momwe udzu wowuma umapsera m’malawi a moto,
momwemonso mizu yawo idzawola
ndipo maluwa awo adzafota ndi kuwuluka ngati fumbi;
chifukwa akana malamulo a Yehova Wamphamvuzonse,
ndipo anyoza mawu a Woyerayo wa Israeli.
25 N’chifukwa chake mkwiyo wa Yehova wayakira anthu ake;
watambasula dzanja lake pa anthuwo ndipo akuwakantha
Mapiri akugwedezeka,
ndipo mitembo ya anthu yangoti mbwee m’misewu ngati zinyalala.

Komabe ngakhale watero, mkwiyo wake sunaleke,
dzanja lake likanali chitambasulire;

26 Yehova wakweza mbendera kuyitana mtundu wa anthu akutali,
akuyitana anthuwo ndi likhweru kuti abwere kuchokera ku mathero a dziko lapansi.
Awo akubwera,
akubweradi mofulumira kwambiri!
27 Palibe ndi mmodzi yemwe amene akutopa kapena kupunthwa,
palibe amene akusinza kapena kugona;
palibe lamba wa m’chiwuno amene akumasuka,
palibe chingwe cha nsapato chimene chaduka.
28 Mivi yawo ndi yakuthwa,
mauta awo onse ndi okoka,
ziboda za akavalo awo n’zolimba ngati mwala wansagalabwi,
magaleta awo ndi aliwiro ngati kamvuluvulu.
29 Kufuwula kwawo kuli ngati kubangula kwa mkango,
amabangula ngati misona ya mkango;
imadzuma pamene ikugwira nyama
ndipo imapita nayo popanda ndi mmodzi yemwe woyipulumutsa.
30 Tsiku limenelo mitundu ya anthu idzabangula

ngati mkokomo wa madzi a m'nyanja.
Ndipo wina akakayang'ana dzikolo
adzangoona mdima ndi zovuta;
ngakhale kuwala kudzasanduka mdima chifukwa cha mitambo.

# 6

*Masomphenya a Yesaya*

1 Chaka chimene mfumu Uziya anamwalira, ndinaona Ambuye atakhala
pa mpando waufumu, wautali ndi wokwezedwa, ndipo mkanjo wawo
unali wautali; kotero kuti unadzaza m'Nyumba ya Yehova. 2 Pamwamba
pawo panayimirira Aserafi, aliyense anali ndi mapiko asanu ndi limodzi:
awiri anaphimba nkhope zawo, awiri anaphimba mapazi awo, ndipo awiri
ankawulukira. 3 Ndipo Aserafiwo amafuwulirana kuti
"Woyera, woyera, woyera Yehova Wamphamvuzonse.
Dziko lonse lapansi ladzaza ndi ulemerero wake."
4 Chifukwa cha kufuwulako maziko a zitseko ndi ziwundo anagwedezeka
ndipo m'Nyumba ya Yehova munadzaza utsi.

5 Tsono ine ndinafuwula kuti, "Tsoka langa ine! Ndatayika! Pakuti
ndine munthu wapakamwa poyipa, ndipo ndimakhala pakati pa anthu
a pakamwa poyipa, ndipo ndi maso anga ndaona mfumu Yehova
Wamphamvuzonse."

6 Pomwepo mmodzi mwa Aserafi aja anawulukira kwa ine ali ndi khala
lamoto m'dzanja lake, khala limene analichotsa ndi mbaniro pa guwa
lansembe. 7 Ndipo anandikhudza pakamwa panga ndi khala lamotolo
nati, "Taona ndakhudza pa milomo yako ndi khalali; kulakwa kwako
kwachotsedwa, machimo ako akhululukidwa."

8 Kenaka ndinamva mawu a Ambuye akuti, "Kodi ndidzatuma yani?
Ndipo ndani adzapite m'malo mwathu?"

Ndipo ine ndinati, "Ndilipo. Tumeni!"

9 Yehova anati, "Pita ndipo ukawawuze anthu awa:
" 'Kumva muzimva, koma osamvetsetsa;
kupenya muzipenya koma osaona kanthu.'
10 Tsono anthu amenewa uwaphe mtima;
uwagonthetse makutu,
ndipo uwatseke m'maso.
Mwina angaone ndi maso awo,
angamve ndi makutu awo,
angamvetse ndi mitima yawo,
kenaka ndi kutembenuka mtima ndi kuchiritsidwa."

11 Pamenepo ine ndinati, "Zimenezo ndi mpaka liti Inu Ambuye?"

Ndipo Iyeyo anandiyankha kuti,
"Mpaka mizinda itasanduka mabwinja
n'kusowa wokhalamo,
mpaka nyumba zitasowa anthu okhalamo,
mpaka dziko litasanduka chipululu ndithu,
12 mpaka Yehova atasamutsira aliyense kutali,
dziko n'kusiyidwa kwathunthu.
13 Ndipo ngakhale chigawo chakhumi cha anthu chitatsala m'dziko,
nachonso chidzawonongedwa.
Koma monga momwe mitengo ya muwanga ndi thundu
imasiyira chitsa pamene ayidula,
chonchonso mbewu yoyera idzatsalira ngati chitsa chotsala m'dziko."

# 7

### *Yesaya Achenjeza Ahazi*

1 Pamene Ahazi mwana wa Yotamu, mdzukulu wa Uziya anali mfumu ya Yuda, Rezini mfumu ya Siriya ndi Peka mwana wa Remaliya, mfumu ya Israeli anabwera kudzathira nkhondo mzinda wa Yerusalemu, koma sanathe kuwugonjetsa.

2 Tsono nyumba ya Davide inawuzidwa kuti, "Dziko la Siriya lagwirizana ndi Efereimu." Choncho mfumu Ahazi ndi anthu ake ananjenjemera, monga momwe mitengo ya m'nkhalango imagwedezekera ndi mphepo.

3 Pamenepo Yehova anawuza Yesaya kuti, "Tuluka, iwe ndi mwana wako Seariyasubu, mupite mukakumane ndi Ahazi kumapeto kwa ngalande yamadzi yochokera ku Dziwe Lakumtunda, pa msewu wopita ku Munda wa mmisiri wochapa nsalu.
4 Ukamuwuze kuti, 'Chenjera, khala phee ndipo usaope. Usataye mtima chifukwa cha zitsa ziwiri zomwe zikufuka, chifukwa cha ukali woopsa wa Rezini ndi Siriya, ndiponso wa Peka mwana wa Remaliya.
5 Mfumu ya Siriya, Efereimu ndi mwana wa Remaliya apangana kuti akuchitire choyipa. Akunena kuti,
6 'Tiyeni tikalimbane ndi Yuda. Tiyeni tiliwononge ndi kuligawa; tiligawane pakati pathu, ndipo tilonge ufumu mwana wa Tabeeli kumeneko.'
7 Komabe zimene akunena Ambuye Yehova ndi izi:

" 'Zimenezo sizidzatheka,
sizidzachitika konse,
8 pakuti Siriya amadalira Damasiko,
ndipo Damasiko amadalira mfumu Rezini basi.
Zisanathe zaka 65
Efereimu adzawonongedwa kotheratu, sadzakhalanso mtundu wa anthu.
9 Dziko la Efereimu limadalira Samariya
ndipo Samariya amadalira mwana wa Remaliya basi.
Mukapanda kulimbika pa chikhulupiriro chanu,
ndithu simudzalimba konse.' "

10 Yehova anayankhulanso ndi Ahazi,
11 "Pempha chizindikiro kwa Yehova Mulungu wako, chikhale chozama ngati manda kapena chachitali ngati mlengalenga."

12 Koma Ahazi anati, "Ine sindipempha; sindikufuna kuyesa Yehova."

13 Apo Yesaya anati, "Imva tsopano, iwe nyumba ya Davide! Kodi sikokwanira kutopetsa anthu? Kodi mudzayeseranso kutopetsa Mulungu wanga?
14 N'chifukwa chake Ambuye mwini adzakupatsani chizindikiro: Onani, namwali adzakhala woyembekezera ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo mwanayo adzamutcha Imanueli.
15 Azidzadya chambiko ndi uchi, mpaka atadziwa kukana choyipa ndi kusankha chabwino.
16 Koma nthawi yokana choyipa ndi kusankha chabwino kwa mwanayo isanafike, mayiko a mafumu awiri amene amakuopsaniwo adzakhala atasanduka bwinja.
17 Yehova adzabweretsa pa inu, pa anthu anu ndiponso pa nyumba ya bambo wanu masiku a mavuto woti sanakhalepo kuyambira tsiku limene Efereimu anapatukana ndi Yuda. Yehova adzabweretsa mfumu ya ku Asiriya."

18 Tsiku limenelo Yehova adzalizira likhweru ntchentche zochokera ku mitsinje yakutali ku Igupto, ndiponso njuchi zochokera ku dziko la Asiriya.
19 Onsewo adzafika ndi kudzakhazikika mu zigwa zozama, m'ming'alu ya matanthwe ndi m'zitsamba zonse zaminga ndiponso ponse pamene

pali malo omwetsera ziweto. 20 Tsiku limenelo Ambuye adzalemba
ganyu ometa ochokera kutsidya kwa Mtsinje, ndiye mfumu ya ku Asiriya,
kudzameta tsitsi lanu la ku mutu ndi la m'miyendo ndi ndevu zomwe.
21 Tsiku limenelo adzangosunga ng'ombe yayikazi yaying'ono ndi mbuzi
ziwiri. 22 Ndipo chifukwa cha kuchuluka kwa mkaka umene ziwetozi
zidzapereka, munthuyo azidzadya chambiko. Aliyense amene adzatsalire
m'dzikomo azidzadya chambiko ndi uchi. 23 Tsiku limenelo, paliponse
pamene panali mitengo ya mpesa 1,000 ndipo mtengo wake ndi wokwana
masekeli asiliva 1,000, padzamera mkandankhuku ndi minga. 24 Anthu
adzapita kumeneko kukachita uzimba ali ndi uta ndi mivi, popeza kuti
m'dziko monsemo mudzakhala mkandankhuku ndi minga. 25 Ndipo
m'mapiri monse m'mene kale munkalimidwa ndi khasu, simudzapitamo
kuopa mkandankhuku ndi minga; malowo adzasanduka odyetserako
ng'ombe ndi nkhosa.

# 8

### *Asiriya, Chida cha Yehova*

1 Yehova anati kwa ine, "Tenga cholembapo chachikulu ndipo ulembepo
malemba odziwika bwino: KUSAKAZA-KWAMSANGA KUFUNKHA-KOFULUMIRA.
2 Ndipo ndidzayitana wansembe Uriya ndi Zekariya mwana wa Yeberekiya
kuti akhale mboni zanga zodalirika."

3 Ndipo ine ndinapita kwa mneneri wamkazi, ndipo anakhala woyem-
bekezera nabala mwana wamwamuna. Ndipo Yehova anati kwa ine,
"Umutche dzina lakuti, 'Kusakaza-Kwamsanga Kufunkha-Kofulumira.'
4 Mwanayo asanayambe kudziwa kuyitana kuti, 'Ababa' kapena 'Amama'
chuma cha Damasiko ndi zofunkha za Samariya zidzatengedwa ndi
mfumu ya ku Asiriya."

5 Yehova anayankhulanso ndi Ine;

6 "Popeza anthu a dziko ili akana
madzi anga oyenda mwachifatse a ku Siloamu,
ndipo akukondwerera Rezini
ndi mwana wa Remaliya,
7 n'chifukwa chake Ambuye ali pafupi kubweretsa
madzi amkokomo a mtsinje wa Yufurate kudzalimbana nawo;
mfumu ya ku Asiriya ndi gulu lake lonse lankhondo.
Madziwo adzasefukira m'ngalande zake zonse
ndi m'magombe ake onse.
8 Ndipo adzalowa mwamphamvu m'dziko la Yuda, adzasefukira,
adzapitirira mpaka kumuyesa m'khosi.
Mapiko ake otambasuka adzaphimba dziko lako lonse,
iwe Imanueli!"

9 Chitani phokoso lankhondo, inu mitundu ya anthu, ndipo munjenjemere!
Tamverani, inu mayiko onse akutali.
Konzekerani nkhondo ndipo munjenjemere!
Konzekerani nkhondo ndipo munjenjemere!
10 Konzani kachitidwe kanu kankhondo, koma simudzaphula kanthu,
kambiranani zochita, koma zidzalephereka,
pakuti Mulungu ali nafe.

### *Yehova Achenjeza Mneneri*

11 Yehova anandiyankhula ine mwamphamvu, ndipo anandichenjeza
kuti ndisamayende m'njira za anthuwa. Iye anati:
12 "Usamanene kuti ndi chiwembu,
chilichonse chimene anthuwa amati ndi chiwembu
usamaope zimene anthuwa amaziopa,
ndipo usamachite nazo mantha.
13 Yehova Wamphamvuzonse ndiye amene uyenera kumuona kuti ndi woyera,
ndiye amene uyenera kumuopa,
ndiye amene uyenera kuchita naye mantha,
14 ndipo ndiye amene adzakhala malo opatulika;
koma kwa anthu a ku Yuda ndi kwa anthu a ku Israeli adzakhala
mwala wopunthwitsa,
mwala umene umapunthwitsa anthu,
thanthwe limene limagwetsa anthu.
Ndipo kwa anthu a mu Yerusalemu adzakhala ngati msampha ndi khwekhwe.
15 Anthu ambiri adzapunthwapo
adzagwa ndi kuthyokathyoka,
adzakodwa ndi kugwidwa."

16 Manga umboniwu
ndipo umate malamulowa pamaso pa ophunzira anga.
17 Ndidzayembekezera Yehova,
amene akubisira nkhope yake nyumba ya Yakobo.
Ine ndidzakhulupirira Iyeyo.
18 Onani, ine ndili pano pamodzi ndi ana amene Yehova wandipatsa,
ndife zizindikiro ndi zodabwitsa kwa Aisraeli zochokera kwa Yehova
Wamphamvuzonse, amene amakhala pa Phiri la Ziyoni.
19 Anthu akakuwuza kuti kafunsire kwa oyankhula ndi mizimu, amene
amayankhula monong'ona ndi mong'ung'udza, kodi anthu sayenera
kukafunsira kwa Mulungu wawo? Chifukwa chiyani amafunsira kwa
anthu akufa m'malo mwa kwa anthu amoyo, 20 kuti akalandireko mawu
enieni ndi malangizo? Ngati anthuwo sayankhula monga mwa mawu
awa, mwa iwo mulibe kuwala. 21 Anthu adzayendayenda m'dziko
movutika kwambiri ali ndi njala; pamene afowokeratu ndi njala, iwo
adzakwiya kwambiri ndipo adzayang'ana kumwamba ndi kutemberera
mfumu yawo ndi Mulungu wawo. 22 Ndipo akadzayang'ana pa dziko
lapansi adzangoona mavuto okhaokha ndi mdima woopsa ndi wodetsa
nkhawa, ndipo adzaponyedwa mu mdima wandiweyani.

# 9

*Ufumu wa Mesiya*

1 Anthu amene anali ndi nkhawa, sadzakhalanso otaya mtima. Masiku
amakedzana Mulungu ananyozetsa dziko la Zebuloni ndi dziko la Nafutali,
koma kutsogolo kuno dera lonse la Galileya, limene lili dziko la anthu
a mitundu ina, kuyambira ku nyanja yayikulu, m'mbali mwa Yorodani,
adzalisandutsa laulemu.
2 Anthu oyenda mu mdima
awona kuwala kwakukulu;
kwa iwo okhala m'dziko la mdima wandiweyani
kuwunika kwawafikira.

3 Inu mwauchulukitsa mtundu wanu
ndipo mwawonjezera chimwemwe chawo.
Iwo akukondwa pamaso panu,
ngati mmene anthu amakondwera nthawi yokolola,
ngatinso mmene anthu amakondwera
pamene akugawana zolanda ku nkhondo.
4 Monga munachitira pogonjetsa Amidiyani,
inu mwathyola goli
limene limawalemera,
ndodo zimene amamenyera mapewa awo,
ndiponso mikwapulo ya anthu owazunza.
5 Nsapato iliyonse ya munthu wankhondo,
ndiponso chovala chilichonse chodonthekera magazi
zidzatenthedwa pa moto
ngati nkhuni.
6 Chifukwa mwana watibadwira,
mwana wamwamuna wapatsidwa kwa ife,
ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lake.
Ndipo adzamutcha dzina lake lakuti
Phungu Wodabwitsa, Mulungu Wamphamvu,
Atate Amuyaya, ndi Mfumu ya Mtendere.
7 Ulamuliro ndi mtendere wake
zidzakhala zopanda malire.
Iye adzalamulira ufumu wake ali pa
mpando waufumu wa Davide,
ndipo adzawukhazikitsa ndi kuwuchirikiza
mwa chiweruzo cholungama ndi pochita zachilungamo
kuyambira nthawi imeneyo mpaka muyaya.
Ndi mtima wake wonse, Yehova Wamphamvuzonse
watsimikiza kuchita zimenezi.

### *Mkwiyo wa Yehova pa Israeli*

8 Ambuye atumiza mawu otsutsa Yakobo;
ndipo mawuwo agwera pa Israeli.
9 Anthu onse okhala mu
Efereimu ndi okhala mu Samariya,
adzadziwa zimenezi.
Iwo amayankhula modzikuza kuti,
10 “Ngakhale njerwa zagumuka,
koma ife tidzamanga ndi miyala yosema.
Mitanda ya mkuyu yagwetsedwa,
koma ife tidzayika mitanda ya mkungudza m’malo mwake.”
11 Koma Yehova wadzutsa adani kuti alimbane nawo
ndipo wawafulumiza adani awo kuti amenyane nawo.
12 Asiriya ochokera kummawa ndi Afilisti ochokera kumadzulo ndipo
ayasama pakamwa kuti adye a Israeli.

Komabe, mkwiyo wake sunawachokere,
mkono wake uli chitambasulire.

13 Koma anthu sanabwerere kwa amene anawakantha uja,
ngakhale kufunafuna Yehova Wamphamvuzonse.
14 Choncho Yehova adzadula mutu wa Israeli pamodzi ndi mchira womwe,

nthambi ya kanjedza ndi bango lomwe tsiku limodzi;
15 mutuwo ndiye akuluakulu ndi olemekezeka,
mchira ndiye aneneri ophunzitsa zabodza.
16 Amene amatsogolera anthuwa ndiwo amawasocheretsa,
ndipo otsogoleredwa amatayika.
17 N'chifukwa chake Ambuye adzakondwera nawo achinyamata,
ngakhale kuwachitira chifundo ana amasiye ndi akazi amasiye,
pakuti aliyense ndi wosapembedza Mulungu ndiponso ndi wochimwa ndipo
aliyense amayankhula zopusa.

Komabe, mkwiyo wake sunawachokere,
mkono wake uli chitambasulire.

18 Ndithu kuyipa kwa anthuwo kumayaka ngati moto;
moto wake umanyeketsa mkandankhuku ndi minga,
umayatsa nkhalango yowirira,
ndipo utsi wake umachita kuti toloo ngati mtambo.
19 Dziko lidzatenthedwa ndi ukali wa Yehova Wamphamvuzonse,
dziko lidzatenthedwa
ndipo anthu adzakhala ngati nkhuni zosonkhera moto;
palibe munthu amene adzachitire chifundo m'bale wake.
20 Kudzanja lamanja adzapeza chakudya n'kudya,
koma adzakhalabe ndi njala;
kudzanja lamanzere adzapeza chakudya n'kudya,
koma sadzakhuta.
Aliyense azidzadya ana ake omwe.
21 Manase adzadya Efereimu ndipo Efereimu adzadya Manase;
onsewa pamodzi adzadya Yuda.

Komabe pa zonsezi, mkwiyo wake sunawachokere,
mkono wake uli chitambasulire.

# 10

1 Tsoka kwa anthu amene amapanga malamulo opanda chilungamo,
kwa iwo amene amalemba zongovutitsa anzawo,
2 kuwalanda anthu osauka ufulu wawo
ndi kumana chilungamo osautsidwa pakati pa anthu anga,
amalanda zinthu za akazi amasiye
ndi kubera ana amasiye.
3 Kodi mudzatani pa tsiku la chilango,
pofika chiwonongeko chochokera kutali?
Kodi mudzathawira kwa yani kuti akuthandizeni?
Nanga chuma chanu mudzachisiya kuti?
4 Kudzatsala n'kungozolika mwamanyazi pakati pa anthu ogwidwa
kapena kufa pamodzi ndi ophedwa.
Komabe pa zonsezi mkwiyo wake sunawachokere,
mkono wake uli chitambasulire.

### *Chiweruzo cha Mulungu pa Asiriya*

5 "Tsoka kwa mfumu ya ku Asiriya, chikwapu cha mkwiyo wanga,
iye ndiye ndodo ya mkwiyo wanga!

6 Ndidzamutuma kukalimbana ndi mtundu wosapembedza Mulungu,
ndidzamutumiza kukalimbana ndi anthu amene amandikwiyitsa Ine,
kukafunkha ndi kulanda chuma,
ndi kuwapondereza pansi ngati matope a m'misewu.
7 Koma izi si zimene akufuna kukachita,
izi si zimene zili m'maganizo mwake;
cholinga chake ndi kukawononga,
kukapulula mitundu yambiri ya anthu.
8 Iye akuti, 'Kodi atsogoleri anga ankhondo si mafumu okhaokha?'
9 'Kodi Kalino sanagonjetsedwe monga Karikemesi?
Kodi Hamati sali ngati Aripadi,
nanga Samariya sali ngati Damasiko?
10 Dzanja langa linakantha maufumu a anthu opembedza mafano,
mafumu amene mafano awo ndi aakulu kupambana Yerusalemu ndi Samariya;
11 nanga Ine n'kulephera kodi kuwononga Yerusalemu pamodzi ndi mafano ake
monga ndinakanthira Samariya pamodzi ndi mafano ake?' "
12 Ambuye akadzamaliza ntchito yonse yolanga phiri la Ziyoni ndi
Yerusalemu adzalanganso mfumu ya ku Asiriya chifukwa cha kudzitama
ndi kunyada kwake. 13 Pakuti mfumuyo ikuti,
" 'Ndachita zimenezi ndi dzanja langa,
ndiponso ndi nzeru zanga, chifukwa ndine wozindikira zinthu.
Ndinachotsa malire a mitundu ya anthu,
ndinafunkha chuma chawo;
ndinagonjetsa mafumu awo monga munthu wamphamvu.
14 Dzanja langa lagwira chuma cha mitundu ya anthu
ngati momwe munthu amagwirira chisa cha mbalame,
ngati momwe anthu amatolera mazira osiyidwa,
motero inenso ndinasonkhanitsa mayiko onse;
palibe mbalame imene inakupiza mapiko ake,
kapena kuyasama kukamwa kuti ilire.' "

15 Kodi nkhwangwa ingathe kudzikuza kupambana woyigwiritsa ntchito,
kapena macheka angathe kudzikuza kupambana wowagwiritsa ntchito?
Ndiye kukhala ngati kuti chikwapu chikuzunguza munthu amene wachinyamula,
kapena ngati kuti ndodo ikuopseza amene wayinyamula!
16 N'chifukwa chake Ambuye Yehova Wamphamvuzonse
adzatumiza matenda owondetsa kwa ankhondo amphamvu;
kunyada kwa mfumuyo kudzapsa
ndi moto wosazima.
17 Mulungu, Kuwala kwa Israeli, adzakhala ngati moto,
Woyera uja wa Israeli adzakhala ngati malawi a moto.
Motowo udzawatentha ndi kuwapsereza
ngati minga ndi mkandankhuku pa tsiku limodzi.
18 Ankhondo ake adzawonongedwa
ngati nkhalango yayikulu
ndi ngati nthaka yachonde.
19 Mitengo yotsalira ya m'nkhalango zake idzakhala yochepa kwambiri,
yoti ndi mwana yemwe ndi kuyiwerenga.

### *Aisraeli Otsala*

20 Tsiku limenelo otsalira a ku Israeli,
opulumuka a nyumba ya Yakobo,
sadzadaliranso anthu
amene anawakantha,
koma adzadalira Yehova,
Woyerayo wa Israeli.
21 Otsalira adzabwerera, otsalira a Yakobo
adzabwerera kwa Mulungu Wamphamvu.
22 Iwe Israeli, ngakhale anthu ako achuluke ngati mchenga wa ku nyanja,
otsala okha ndiwo adzabwerere.
Chiwonongeko chalamulidwa,
chidzaonetsa chilungamo chosefukira.
23 Ambuye Yehova Wamphamvuzonse adzawononga ndithu dziko lonse
monga momwe analamulira.
24 N'chifukwa chake, Ambuye Yehova Wamphamvuzonse akunena kuti,
"Inu anthu anga okhala mu Ziyoni,
musawaope Asiriya,
amene amakukanthani ndi ndodo
nakumenyani ndi zibonga monga mmene Igupto anachitira.
25 Patsala pang'onong'ono kuti mkwiyo wanga uchoke pa inu
ndipo ndidzaonetsa ukali wanga pa iwo mpaka kuwawononga."

26 Yehova Wamphamvuzonse adzawakwapula ndi chikwapu,
monga momwe anakwapulira Amidiyani ku thanthwe la Orebu;
ndipo adzatukula ndodo yake pa madzi
ndikuwalanga monga analangira Igupto pa nyanja.
27 Tsiku limenelo katundu wawo adzachotsedwa pa mapewa anu,
goli lawo lidzachoka m'khosi mwanu;
golilo lidzathyoka
chifukwa cha kunenepa kwambiri.

28 Adani alowa mu Ayati
apyola ku Migironi;
asunga katundu wawo ku Mikimasi.
29 Adutsa pa mpata uja, ndipo akuti,
"Tikagona ku Geba"
Rama akunjenjemera;
Gibeya, mzinda wa Saulo ukuthawa.
30 Lilani mokweza, inu anthu a ku Galimu!
Tchera khutu, iwe Laisa!
Iwe Anatoti wosauka!
31 Anthu a ku Madimena akuthawa;
anthu a ku Gebimu bisalani.
32 Lero lomwe lino adaniwo adzayima ku Nobu;
adzagwedeza mikono yawo,
kuopseza anthu a ku Ziyoni,
pa phiri la Yerusalemu.

33 Taonani, Ambuye Yehova Wamphamvuzonse,
adzadula mwamphamvu nthambi za mitengo,
mitengo yodzikweza idzadulidwa,
mitengo yayitali idzagwetsedwa.

34 Yehova adzadula ndi nkhwangwa mitengo ya m'nkhalango yowirira;
Lebanoni adzagwa pamaso pa Wamphamvu.

# 11

*Za Ufumu Wamtendere wa Mesiya*

1 Padzatuluka mphukira pa tsinde la Yese
ndipo nthambi idzaphukira kuchokera ku mizu yake.
2 Mzimu wa Yehova udzakhala pa iye
Mzimu wanzeru ndi wa kumvetsa zinthu,
Mzimu wauphungu ndi wamphamvu,
Mzimu wachidziwitso ndi wakuopa Yehova.
3 Ndipo kuopa Yehova ndiye chidzakhale chinthu chomukondweretsa.

Iye sadzaweruza potsata zooneka pamaso,
kapena kugamula mlandu potsata zakumva;
4 koma amphawi adzawaweruza mwachilungamo,
adzaweruza mwachilungamo mlandu wa anthu osauka a dziko lapansi.
Iye adzakantha dziko lapansi ndi mawu ake;
atalamula Iyeyu anthu oyipa adzaphedwa.
5 Chilungamo chidzakhala ngati lamba wake
ndipo kukhulupirika kudzakhala ngati chomangira m'chiwuno mwake.

6 M'mbulu udzakhala pamodzi ndi mwana wankhosa,
kambuku adzagona pansi pamodzi ndi mwana wambuzi,
mwana wang'ombe ndi mwana wa mkango adzadyera limodzi
ndipo mwana wamng'ono adzaziweta.
7 Ng'ombe yayikazi ndi chimbalangondo zidzadya pamodzi,
ana awo adzagona pamodzi,
ndipo mkango udzadya udzu ngati ng'ombe.
8 Mwana wakhanda adzasewera pa dzenje la mamba,
ndipo mwana wamng'ono adzapisa dzanja lake ku phanga la mphiri osalumidwa.
9 Sipadzakhala chilichonse chopweteka kapena chowononga
pa phiri lopatulika la Yehova,
pakuti anthu a dziko lapansi adzadzaza ndi nzeru yotha kudziwa Yehova
monga momwe nyanja imadzazira ndi madzi.

10 Tsiku limenelo mfumu yatsopano yochokera pa Muzu wa Yese
idzakhala ngati chizindikiro kwa anthu a mitundu yonse. Mitundu
ya anthu idzasonkhana kwa Iye, ndipo malo awo okhalapo adzakhala
aulemerero. 11 Tsiku limenelo Ambuye adzatambasula dzanja lake
kachiwiri kuti awombole anthu ake otsalira ku Asiriya, ku Igupto, ku
Patirosi, Kusi, ku Elamu, ku Sinana, ku Hamati ndi pa zilumba za nyanja
yamchere.

12 Adzakwezera mitundu ya anthu mbendera,
ndipo adzasonkhanitsa otayika a ku Israeli;
Iye adzasonkhanitsa anthu obalalika a ku Yuda
kuchokera ku mbali zonse zinayi za dziko lapansi.
13 Nsanje ya Efereimu idzatha,
ndipo adani a Yuda adzatha;
Efereimu sadzachitira nsanje Yuda,

ngakhale Yuda sadzamuda Efereimu.
14 Yuda ndi Efereimu adzathira nkhondo pa Afilisti mbali ya kumadzulo;
ndipo onsewo pamodzi adzalanda zinthu za anthu a kummawa.
Adzalimbana ndi Edomu ndi Mowabu,
ndipo Aamoni adzawagonjera.
15 Yehova adzaphwetsa
mwendo wa nyanja ya Igupto;
adzatambasula dzanja lake ndipo adzawombetsa mphepo yotentha
pa mtsinje wa Yufurate.
Iye adzawugawa mtsinjewo kukhala timitsinje tisanu ndi tiwiri
kuti anthu athe kuwoloka powuma atavala nsapato.
16 Padzakhala msewu waukulu woti ayendepo anthu ake otsalira
amene anatsalira ku Asiriya,
monga mmene panali msewu waukulu woyendapo Israeli
pamene amachokera ku Igupto.

# 12

*Nyimbo za Mayamiko*

1 Tsiku limenelo aliyense wa inu adzati:
"Ndikukuyamikani, Inu Yehova;
chifukwa ngakhale munandipsera mtima,
mkwiyo wanu wachoka,
ndipo mwanditonthoza.
2 Zoonadi, Mulungu ndiye Mpulumutsi wanga;
ndidzamudalira ndipo sindidzachita mantha.
Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga;
Iye wakhala chipulumutso changa."
3 Mudzakondwera popeza Yehova
ali ngati chitsime cha chipulumutso chanu.
4 Tsiku limenelo mudzati:
"Yamikani Yehova, tamandani dzina lake;
mulengeze ntchito zake pakati pa mitundu ya anthu,
ndipo mulalike kuti dzina lake ndi lopambana.
5 Imbirani Yehova, pakuti wachita ntchito zazikulu;
zimenezi zidziwike pa dziko lonse lapansi.
6 Fuwulani ndi kuyimba mwachimwemwe, inu anthu a ku Ziyoni;
pakuti Woyerayo wa Israeli ndi wamkulu pakati panu."

# 13

*Kulangidwa Kwa Babuloni*

1 Uthenga onena za Babuloni umene Yesaya mwana wa Amozi anawu-
landira:
2 Kwezani mbendera yankhondo pa phiri loti see,
muwafuwulire ankhondo;
muwakodole kuti adzalowe pa zipata
za anthu olemekezeka.
3 Ine Yehova, ndalamulira ankhondo anga;
ndasonkhanitsa ankhondo anga kuti akhale zida zanga zolangira
amene amadzikuza ndi chipambano changa.

4 Tamvani phokoso ku mapiri,

likumveka ngati phokoso la gulu lalikulu la anthu!
Tamvani phokoso pakati pa maufumu,
ngati kuti mitundu ya anthu ikusonkhana pamodzi!
Yehova Wamphamvuzonse akukhazika asilikali ake mokonzekera
kuchita nkhondo.
5 Iwo akuchokera ku mayiko akutali,
kuchokera kumalekezero a dziko
Yehova ali ndi zida zake za nkhondo
kuti adzawononge dziko la Babuloni.

6 Lirani mofuwula, pakuti tsiku la Yehova layandikira;
lidzabwera ngati chiwonongeko chochokera kwa Wamphamvuzonse.
7 Zimenezi zinafowoketsa manja onse,
mtima wa munthu aliyense udzachokamo.
8 Anthu adzagwidwa ndi mantha aakulu,
zowawa ndi masautso zidzawagwera;
adzamva zowawa zonga amamva mayi pobereka.
Adzayang'anana mwamantha,
nkhope zawo zikufiira ngati malawi amoto.

9 Taonani, tsiku la Yehova likubwera,
tsiku lopanda chisoni, lawukali ndi lamkwiyo;
kudzasandutsa dziko kuti likhale chipululu
ndi kuwononga anthu ochimwa a m'menemo.
10 Nyenyezi zakumwamba ndiponso zonse zamlengalenga
sizidzaonetsa kuwala kwawo.
Dzuwa lidzada potuluka,
ndipo mwezi sudzawala konse.
11 Ndidzalanga dziko lonse chifukwa cha zolakwa zake,
anthu oyipa ndidzawalanga chifukwa cha machimo awo.
Ndidzathetsa kunyada kwa odzikuza,
ndipo ndidzatsitsa kudzitukumula kwa anthu ankhanza.
12 Ndidzasandutsa anthu kukhala ovuta kupeza kuposa mmene amasowera golide wabwino.
Iwo sazidzapezekapezeka kuposa mmene amasowera golide wa ku Ofiri.
13 Tsono ndidzagwedeza miyamba
ndipo dziko lapansi lidzachoka pa maziko ake.
Izi zidzachitika chifukwa cha ukali wa Wamphamvuzonse
pa tsiku la mkwiyo wake woopsa.

14 Ngati mbawala zosakidwa,
ngati nkhosa zopanda wozikusa,
munthu aliyense adzabwerera kwa anthu akwawo,
aliyense adzathawira ku dziko lake.
15 Aliyense amene atadzapezeke ndi kugwidwa
adzaphedwa momubaya ndi lupanga.
16 Ana awo akhanda adzaphwanyidwa iwo akuona;
nyumba zawo zidzafunkhidwa ndipo akazi awo adzagwiriridwa.

17 Taona, Ine ndidzadzutsa Amedi amene safuna siliva
ndipo sasangalatsidwa ndi golide,

kuti amenyane ndi Ababuloni.
18 Adzapha anyamata ndi mauta awo;
sadzachitira chifundo ana
ngakhale kumvera chisoni ana akhanda.
19 Babuloni, ufumu wake ndi waulemerero kuposa mafumu onse.
Anthu ake amawunyadira.
Koma Yehova adzawuwononga
ngati mmene anawonongera Sodomu ndi Gomora.
20 Anthu sadzakhalamonso
kapena kukhazikikamo pa mibado yonse;
palibe Mwarabu amene adzayimike tenti yake,
palibe m'busa amene adzawetamo ziweto zake.
21 Koma nyama zakuthengo ndizo zidzakhale kumeneko,
nyumba zake zidzadzaza ndi nkhandwe;
mu mzindamo muzidzakhala akadzidzi,
ndipo atonde akuthengo azidzalumphalumphamo.
22 Mu nsanja zake muzidzalira afisi,
m'nyumba zake zokongola muzidzalira nkhandwe.
Nthawi yake yayandikira
ndipo masiku ake ali pafupi kutha.

# 14

1 Yehova adzachitira chifundo Yakobo;
adzasankhanso Israeli
ndi kuwalola kuti akhalenso m'dziko lawo.
Alendo adzabwera kudzakhala nawo
ndi kudziphatika okha kukhala ngati a m'nyumba ya Yakobo.
2 Anthu a mitundu ina adzaperekeza a Israeli
ku dziko lawo.
Tsono Aisraeli adzasandutsa anthu a mitundu ina aja
kukhala antchito awo aamuna ndi aakazi m'dziko la Yehova.
Ndiye kuti Aisraeli adzasandutsa akapolo anthu amene kale anali ambuye awo.
Iwo adzasandutsa akapolo anthu amene kale ankawalamulira ndi kuwazunza.
3 Yehova akadzakupumitsani ku zowawa ndi mavuto, ndiponso
kuntchito yakalavulagaga imene ankakugwiritsani, 4 mudzayankhula
monyogodola mfumu ya Babuloni kuti,
Wopsinja uja watha!
Ukali wake uja watha!
5 Yehova wathyola chikwapu cha anthu oyipa,
Iye waphwanya ndodo ya olamulira.
6 Mfumu ya ku Babuloni inkakantha mitundu ya anthu mwaukali
powamenya kosalekeza,
Iyo inkagonjetsa anthu a mitundu ina mwaukali
ndikuwazunza kosalekeza.
7 Koma tsopano mayiko onse ali pa mpumulo ndi pa mtendere;
ndipo akuyimba mokondwa.
8 Ngakhale mitengo ya payini ndi mikungudza ya ku Lebanoni
ikuyimba za iwe mokondwa ndipo ikuti,
"Chigwetsedwere chako pansi,
palibe wina anabwera kudzatigwetsa."

9 Ku manda kwatekeseka
kuti akulandire ukamabwera;
mizimu ya anthu akufa, aja amene anali atsogoleri
a dziko lapansi, yadzutsidwa.
Onse amene anali mafumu a mitundu ya anthu
ayimiritsidwa pa mipando yawo.
10 Onse adzayankha;
adzanena kwa iwe kuti,
“Iwenso watheratu mphamvu ngati ife;
Iwe wafanana ndi ife.”
11 Ulemerero wako wonse walowa m’manda,
pamodzi ndi nyimbo za azeze ako;
mphutsi zayalana pogona pako
ndipo chofunda chako ndi nyongolotsi.

12 Wagwa pansi bwanji kuchoka kumwamba,
iwe nthanda, mwana wa m’bandakucha!
Wagwetsedwa pansi pa dziko lapansi,
Iwe amene unagonjetsapo mitundu ya anthu!
13 Mu mtima mwako unkanena kuti,
“Ndidzakwera mpaka kumwamba;
ndidzakhazika mpando wanga waufumu
pamwamba pa nyenyezi za Mulungu;
ndidzakhala pa mpando waufumu pa phiri losonkhanirako,
pamwamba penipeni pa phiri la kumpoto.
14 Ndidzakwera pamwamba pa mitambo;
ndidzafanana ndi Wammwambamwamba.”
15 Koma watsitsidwa m’manda
pansi penipeni pa dzenje.

16 Anthu akufa adzakupenyetsetsa
nadzamalingalira za iwe n’kumati,
“Kodi uyu ndi munthu uja anagwedeza dziko lapansi
ndi kunjenjemeretsa maufumu,
17 munthu amene anasandutsa dziko lonse chipululu,
amene anagwetsa mizinda yake
ndipo sankalola kuti anthu ogwidwa abwerere kwawo?”

18 Mafumu onse a mitundu ya anthu akugona mwaulemu
aliyense m’manda akeake.
19 Koma iwe watayidwa kunja kwa manda ako,
ngati nthambi yowola ndi yonyansa.
Mtembo wako waphimbidwa ndi anthu ophedwa;
amene anabayidwa ndi lupanga,
anatsikira m’dzenje lamiyala
ngati mtembo woponderezedwa.
20 Sudzayikidwa nawo m’manda mwaulemu,
chifukwa unawononga dziko lako
ndi kupha anthu ako.

Zidzukulu za anthu oyipa
sizidzakumbukika n’pang’ono pomwe.

21 Konzani malo woti muphere ana ake aamuna
chifukwa cha machimo a makolo awo;
kuti angadzuke ndi kulanda dziko lapansi
ndi kulidzaza dziko lonselo ndi mizinda yawo.

22 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Ine ndidzathira nkhondo mzinda wa Babuloni.
Ndidzachotseratu mu Babuloni dzina lake ndi onse otsaliramo.
Ndiye kuti sipadzakhala ana kapena zidzukulu,"
akutero Yehova.
23 "Ndidzawusandutsa mzindawo malo okhalamo anungu
ndiponso dambo lamatope;
ndidzawusesa ndi tsache lowononga,"
akutero Yehova Wamphamvuzonse.

### *Za Kulangidwa kwa Asiriya*

24 Yehova Wamphamvuzonse walumbira kuti,
"Ndithudi, monga ndaganizira ndidzachitadi choncho,
ndipo monga momwe ndatsimikizira zidzakhala momwemo ndithu.
25 Ndidzawawononga Asiriya m'dziko langa;
ndidzawapondereza ndi mapazi pa mapiri anga;
ndidzachotsa goli lawo pa anthu anga,
ndipo ndidzachotsa katundu wawo pa mapewa awo."

26 Izi ndizo ndakonza kuti zichitike pa dziko lonse lapansi,
ndatambasula dzanja pa anthu a mitundu yonse.
27 Pakuti Yehova Wamphamvuzonse watsimikiza, ndipo ndani angamuletse?
Dzanja lake latambasulidwa ndipo ndani angalibweze?

### *Za Kulangidwa kwa Afilisti*

28 Uthenga uwu unabwera chaka chimene mfumu Ahazi anamwalira:
29 Musakondwere inu Afilisti nonse
kuti Asiriya amene anali ngati ndodo yokukanthani anathedwa;
chifukwa kuchokera ku njoka yomweyi (mfumu ya Aasiriya) mudzatuluka mphiri,
ndipo chipatso chake chidzakhala njoka yaliwiro ndiponso yaululu.
30 Osaukitsitsa adzapeza chakudya
ndipo amphawi adzakhala mwamtendere.
Koma anthu ako ndidzawawononga ndi njala,
ndipo njalayo idzapha ngakhale opulumuka ako.

31 Lirani kwambiri, anthu a pa chipata! Fuwulani kwambiri, anthu a mu mzinda!
Njenjemerani ndi mantha, inu Afilisti nonse!
Mtambo wa utsi ukuchokera kumpoto,
ndipo palibe wamantha pakati pa ankhondo ake.
32 Kodi tidzawayankha chiyani
amithenga a ku Filisitiya?
"Yehova wakhazikitsa Ziyoni,
ndipo mu mzinda wakewu, anthu ozunzika apeza populumukira."

# 15

### *Za Kulangidwa kwa Mowabu*

1 Uthenga wonena za Mowabu:
Popeza kuti mu usiku umodzi wokha mzinda wa Ari wa ku Mowabu wawonongedwa,
wawonongedwa pa usiku umodzi wokha.
Mzinda wa Kiri wawonongedwa,
wawonongedwa pa usiku umodzi wokha.
2 Anthu a ku Diboni akupita ku nyumba ya milungu yawo,
akupita ku malo awo achipembedzo kukalira;
anthu a ku Mowabu akulirira mofuwula mzinda wa Nebo ndi wa Medeba.
Mutu uliwonse wametedwa mpala,
ndipo ndevu zonse zametedwa.
3 M'misewu akuvala ziguduli;
pa madenga ndi m'mabwalo
aliyense akulira mofuwula,
misozi ili pupupu.
4 Anthu a ku Hesiboni ndi Eleali akulira mofuwula,
mawu awo akumveka mpaka ku Yahazi.
Kotero asilikali a ku Mowabu akulira mofuwula,
ndipo ataya mtima.

5 Inenso ndikulirira Mowabu;
chifukwa othawa nkhondo ake akupita akulira ku chikweza cha Luluti mpaka ku Zowari
ndi Egilati-Selisiya
akupita akulira ku chikweza cha Luhiti,
Akulira mosweka mtima
pa njira yopita ku Horonaimu;
akulira mosweka mtima chifukwa cha chiwonongeko chawo.
6 Madzi a ku Nimurimu aphwa
ndipo udzu wauma;
zomera zawonongeka
ndipo palibe chomera chobiriwira chatsala.
7 Kotero kuti chuma chomwe anachipeza ndi kuchisunga,
achitenga kuti awoloke nacho chigwembe cha Misondozi.
8 Kulira kwawo kukumveka m'dziko lonse la Mowabu;
kulira kwawo kosweka mtima kukumveka
mpaka ku Egilaimu ndi Beeri-Elimu.
9 Madzi a ku Dimoni afiira ndi magazi,
komabe ndidzabweretsa zina zambiri pa Dimoni,
mkango woti udzagwire aliyense othawa mu Mowabu
ndi aliyense wotsala m'dzikomo.

# 16

1 Anthu a ku Mowabu
atumiza mphatso za ana ankhosa onenepa,
kuchokera ku Sela kudutsa chipululu
mpaka kukafika ku phiri la Ziyoni.
2 Monga momwe mbalame zimawulukira uku ndi uku
akazimwaza m'chisa,

momwemonso akazi a ku Mowabu
akuyendayenda ku madooko a Arinoni.

3 Amowabu aja anawuza a ku Yuda kuti,
“Tiwuzeni chochita, gamulani zoti tichite.
Inu mutiteteze kwa adani anthu.
Mukhale ngati mthunzi wathu dzuwa lili pa liwombo.
Mutibise,
musatipereke ife othawa nkhondo kwa adani athu.
4 Lolani kuti anthu othawa nkhondo a ku Mowabu azikhala pakati panu;
mukhale populumukira pawo kwa wowononga.”

Nthawi idzafika ndipo wozunzayo sadzakhalaponso,
kuwononga kudzaleka;
waukaliyo adzachoka m’dzikomo.
5 Mpando waufumu udzakhazikitsidwa mwachikondi;
mmodzi mwa zidzukulu za Davide adzakhalapo mokhulupirika.
Iyeyo poweruza adzatsata chilungamo
ndipo adzalimbikitsa kuchita zachilungamo.

6 Tinamva kuti Mowabu anadzikuza kwambiri.
Kunyada kwawo
ndi kunyogodola kwawo ndi kudzitama kwawo,
zonse ndi zopanda phindu.
7 N’chifukwa chake Amowabu akulira kwambiri;
iwo akulirira dziko lawo.
Akubuma momvetsa chisoni
chifukwa cha makeke a mphesa a ku Kiri Hareseti.
8 Minda ya ku Hesiboni yauma,
minda ya mpesa ya ku Sibina yaguga.
Atsogoleri a mitundu ina anapondaponda
minda ya mpesa wabwino,
imene nthambi zake zinakafika ku Yazeri,
mpaka kutambalalira ku chipululu.
Mizu yake inakafika
mpaka ku tsidya la nyanja.
9 Kotero Ine ndikulira, monga mmene akulirira anthu a ku Yazeri,
chifukwa cha minda ya mpesa ya ku Sibima.
Inu anthu a ku Hesiboni, inu anthu a ku Eleali,
ndikukunyowetsani ndi misozi!
Mwalephera kupeza zokolola,
chifukwa cha nkhondo imene inawononga zokolola zonse.
10 Chimwemwe ndi chisangalalo zalekeka ku minda yanu ya zipatso;
palibe amene akuyimba kapena kufuwula m’minda ya mpesa;
palibe amene akupsinya vinyo ku malo opsinyira mphesa,
pakuti ndathetsa kufuwula.
11 Chifukwa chake moyo wanga ukulira ngati pangwe kulirira Mowabu,
mtima wanga ukubuwula chifukwa cha Kiri Hareseti.
12 Ngakhale anthu a ku Mowabu
apite ku malo awo achipembedzo
koma amangodzitopetsa ndi kutaya nthawi chabe
chifukwa sizidzatheka.

13 Awa ndi mawu amene Yehova wayankhula kale zokhudza Mowabu.
14 Koma tsopano Yehova akuti, “Zisanathe zaka zitatu, potsata m’mene munthu waganyu amawerengera, ulemerero wa Mowabu udzakhala utatheratu ndipo anthu ake ambiri adzakhala atawonongeka, ndipo opulumuka ake adzakhala ochepa ndi ofowoka.”

# 17

*Uthenga Wotsutsa Damasiko*

1 Uthenga wonena za Damasiko:
“Taonani, mzinda wa Damasiko sudzakhalanso mzinda,
koma udzasanduka bwinja.
2 Mizinda ya Aroeri idzakhala yopanda anthu
ndipo idzakhala ya ziweto, zimene zidzagona pansi
popanda wina woziopseza.
3 Ku Efereimu sikudzakhalanso linga,
ndipo ku Damasiko sikudzakhalanso ufumu;
Otsalira a ku Siriya adzachotsedwa ulemu
monga anthu a ku Israeli,”
akutero Yehova Wamphamvuzonse.

4 “Tsiku limenelo ulemerero wa Yakobo udzazimirira;
ndipo chuma chake chidzasanduka umphawi.
5 Israeli adzakhala ngati munda wa tirigu
umene anatsiriza kukolola.
Adzakhalanso ngati munda wa m’chigwa cha Refaimu
anthu atatha kukunkha ngala za tirigu.
6 Komabe Aisraeli ochepa okha ndiwo ati adzatsale
monga m’mene zimatsalira zipatso ziwiri kapena zitatu pa nthambi ya pamwamba penipeni
kapena zipatso zisanu pa nthambi za m’munsi
mwa mtengo wa olivi akawugwedeza,”
akutero Yehova, Mulungu wa Israeli.

7 Tsiku limenelo anthu adzayang’ana Mlengi wawo
ndipo adzatembenukira kwa Woyerayo wa Israeli.
8 Iwo sadzakhulupiriranso maguwa ansembe,
ntchito ya manja awo,
ndipo sadzadaliranso mitengo ya mafano a Asera,
ndiponso maguwa ofukizirapo lubani amene manja awo anapanga.
9 Tsiku limenelo mizinda yawo yamphamvu, imene anasiya chifukwa
cha Aisraeli, idzakhala ngati malo osiyidwa kuti awirire ndi kumera
ziyangoyango. Ndipo yonse idzakhala mabwinja.
10 Inu mwayiwalatu Mulungu Mpulumutsi wanu;
simunakumbukire Thanthwe, linga lanu.
Choncho, ngakhale munadzala mbewu zabwino,
ndi kuyitanitsa kunja mitengo ya mpesa,
11 nimuyembekeza kuti zikule tsiku lomwelo
ndi kuphukira maluwa mmawa mwake,
komabe zimenezi sizidzakupindulirani
pa tsiku la mavuto.

12 Aa, mkokomo wa anthu a mitundu yambiri,

akusokosa ngati kukokoma kwa nyanja!
Aa, phokoso la anthu a mitundu ina,
akusokosa ngati mkokomo wa madzi amphamvu!
13 Ngakhale ankhondo a mitundu ina akubwera ndi mkokomo ngati wa madzi ambiri,
koma adzathawira kutali Mulungu akadzawadzudzula.
Yehova adzawapirikitsa ngati mankhusu owuluka ndi mphepo pa phiri,
ndi ngati fumbi la kamvuluvulu asanayambe.
14 Pofika nthawi yamadzulo zoopsa zidzayamba kuchitika,
ndipo zidzakhala zitatha pofika mmawa.
Izi ndizo zidzachitikire anthu otilanda zinthu,
gawo la amene amatibera zinthu zathu.

# 18

*Za Kulangidwa kwa Kusi*

1 Tsoka kwa anthu a ku Kusi.
Kumeneko kumamveka mkokomo wa mapiko a dzombe.
2 Dziko limenelo limatumiza akazembe pa mtsinje wa Nailo,
m'mabwato amabango amene amayandama pa madzi,
ndikunena kuti, "Pitani, inu amithenga aliwiro,
kwa mtundu wa anthu ataliatali a khungu losalala,
ndi woopedwa ndi anthu.
Akazembe anatumidwa ku dziko la anthu amphamvu ndi logonjetsa anthu ena.
Dziko lawo ndi logawikanagawikana ndi mitsinje."

3 Inu nonse anthu a pa dziko lonse,
inu amene mumakhala pa dziko lapansi,
pamene mbendera yakwezedwa pa mapiri
yang'anani,
ndipo pamene lipenga lilira
mumvere.
4 Pakuti Yehova akunena kwa ine kuti,
"Ndili chikhalire ku malo anga kuno, ndidzakhala chete, ndi kumangoyang'ana,
monga momwe dzuwa limawalira nthawi yotentha,
monganso momwe mame amagwera usiku pa nthawi yotentha yokolola."
5 Pakuti, anthu asanayambe kukolola, maluwa atayoyoka
ndiponso mphesa zitayamba kupsa,
Iye adzadula mphukira ndi mipeni yosadzira,
ndipo adzadula ndi kuchotsa nthambi zotambalala.
6 Mitembo ya anthu ankhondo adzasiyira mbalame zam'mapiri zodya nyama
ndiponso zirombo zakuthengo;
mbalame zidzadya mitemboyo nthawi yonse ya chilimwe,
ndipo zirombo zidzayidya pa nthawi yonse yachisanu.
7 Pa nthawi imeneyo anthu adzabwera ndi mphatso kwa Yehova Wamphamvuzonse,
zochokera kwa anthu ataliatali ndi osalala,
kuchokera kwa mtundu wa anthu woopedwa ndi anthu apafupi ndi akutali omwe,
mtundu wa anthu amphamvu ndi a chiyankhulo chachilendo,

anthu amene dziko lawo ndi logawikanagawikana ndi mitsinje.
Adzabwera nazo mphatso ku Phiri la Ziyoni, ku malo a Dzina la Yehova Wamphamvuzonse.

# 19

### *Za Kulangidwa kwa Igupto*

1 Uthenga onena za Igupto:
Taonani, Yehova wakwera pa mtambo waliwiro,
ndipo akupita ku Igupto.
Mafano a ku Igupto akunjenjemera pamaso pake,
ndipo mitima ya Aigupto yachokamo ndi mantha.

2 "Ine ndidzadzutsa Aigupto kuti amenyane okhaokha;
m'bale adzamenyana ndi m'bale wake,
mnansi ndi mnansi wake,
mzinda ndi mzinda unzake,
ndiponso ufumu ndi ufumu unzake.
3 Aigupto adzataya mtima
popeza ndidzalepheretsa zolinga zawo;
adzapempha nzeru kwa mafano awo ndiponso kwa woyankhula ndi mizimu ya anthu akufa,
kwa amawula ndi kwa oyankhula ndi mizimu.
4 Ndidzawapereka Aigupto
kwa olamulira ankhanza,
ndipo mfumu yoopsa idzawalamulira,"
akutero Ambuye Yehova Wamphamvuzonse.

5 Madzi a mu mtsinje wa Nailo adzaphwa,
ndipo m'mbali mwa mtsinje mudzang'aluka ndi kuwuma.
6 Ngalande zake zidzanunkha;
ndipo mitsinje ya Igupto idzayamba kuchepa ndi kuwuma.
Bango ndi dulu zidzafota,
7 ndiponso zomera za m'mphepete mwa Nailo
ndi ku mathiriro a mtsinjewo.
Zonse zodzalidwa m'mbali mwa Nailo
zidzawuma, zidzawuluzika ndipo sizidzaonekanso.
8 Asodzi adzabuwula ndi kudandaula,
onse amene amaponya mbedza mu Nailo;
onse amene amaponya makoka m'madzi
adzalira.
9 Amene amagwira ntchito yopota thonje adzataya mtima,
anthu oluka nsalu zofewa zabafuta adzataya chiyembekezo.
10 Akatswiri opanga nsalu adzangoti kakasi,
ndipo anthu onse ogwira ntchito yolipidwa adzatheratu mphamvu.

11 Akuluakulu a ku Zowani ndi zitsiru;
aphungu a nzeru a Farao amalangiza zopusa.
Kodi mungathe kunena bwanji kwa Farao kuti,
"Ine ndine mmodzi mwa anthu anzeru,
wophunzira wa mafumu akale?"

12 Iwe Farao, anthu ako anzeru ali kuti?

Abweretu kuti akuwuze ndi kukudziwitsa
zimene Yehova Wamphamvuzonse
wakonza kuchitira dziko la Igupto.
13 Akuluakulu a ku Zowani asanduka zitsiru,
atsogoleri a ku Mefisi anamizidwa;
atsogoleri a dziko la Igupto
asocheretsa anthu a dzikolo.
14 Yehova wasocheretsa
anthu a ku Igupto.
Iwo akuchita kudzandira pa zonse zimene akuchita,
ngati chidakwa choterereka pa masanzi ake.
15 Palibe chimene munthu wa mu Igupto angachite,
mtsogoleri kapena wotsatira, nthambi ya kanjedza kapena bango.

16 Tsiku limenelo Aigupto adzakhala ngati amayi. Adzanjenjemera ndi kuchita mantha akadzaona Yehova Wamphamvuzonse, atakweza dzanja
lake kufuna kuwalanga. 17 Ndipo dziko la Yuda lidzaopsa dziko la
Aigupto. Aliyense amene adzamve dzina la Yuda adzaopsedwa chifukwa cha zimene Yehova Wamphamvuzonse wakonzekera kuchitira dziko la Igupto.

18 Tsiku limenelo ku dziko la Igupto kudzakhala mizinda isanu yoyankhula chiyankhulo cha Akanaani, ndipo anthu ake adzalumbira kwa Yehova Wamphamvuzonse kuti adzamutumikira. Umodzi mwa mizindayo udzatchedwa Mzinda Wachilungamo.

19 Tsiku limenelo m'kati mwa dziko la Igupto mudzakhala guwa lansembe la Yehova, ndipo m'malire mwake adzayikira Yehova mwala
wachikumbutso. 20 Zimenezo zidzakhala umboni wozindikiritsa kuti Yehova Wamphamvuzonse alimo m'dziko la Igupto. Pamene Aigupto adzalirira Yehova chifukwa cha owapondereza, Iye adzawatumizira mpu-
lumutsi ndi mtetezi ndipo adzawalanditsa. 21 Kotero Yehova adzadziulula
yekha kwa Aigupto, ndipo tsiku limenelo adzadziwa Yehova. Adzapembedza Yehova popereka nsembe ndi popereka zopereka zachakudya;
Adzalumbira kwa Yehova ndipo adzachita zimene alumbirazo. 22 Yehova
adzakantha Aigupto ndi mliri. Iye adzawakanthadi ndipo kenaka adzawachiritsa. Aigupto adzatembenukira kwa Yehova ndipo Iye adzamva madandawulo awo ndi kuwachiritsa.

23 Tsiku limenelo kudzakhala msewu waukulu wochoka ku Igupto kupita ku Asiriya. Aasiriya adzapita ku Igupto ndi Aigupto ku Asiriya. Aigupto
ndi Aasiriya adzapembedza pamodzi. 24 Tsiku limenelo Israeli adzakhala
pamodzi ndi Igupto ndi Asiriya, mayiko atatuwa adzakhala dalitso pa
dziko lapansi. 25 Yehova Wamphamvuzonse adzawadalitsa, ndi mawu awa, "Adalitsike anthu anga Aigupto, Aasiriya, ntchito ya manja anga, ndi Aisraeli osankhidwa anga."

# 20

*Za Chilango cha Igupto ndi Kusi*

1 M'chaka chimene mkulu wankhondo wotumidwa ndi mfumu ya ku Asiriya, anabwera ku Asidodi ndi kuwuthira nkhondo ndi kuwulanda,
2 nthawi imeneyo Yehova anawuza Yesaya mwana wa Amozi kuti, "Pita kavule chiguduli ndi nsapato zako." Ndipo iye anaterodi, ankangoyenda wamaliseche ndiponso wopanda nsapato.

3 Kenaka Yehova anati, "Monga momwe mtumiki wanga Yesaya wakhala akuyendera wamaliseche ndiponso wopanda nsapato kwa zaka

zitatu ngati chizindikiro ndi chenjezo kwa dziko la Igupto ndi Kusi,
4 momwemonso mfumu ya ku Asiriya idzatenga ukapolo anthu a ku Igupto
ndi a ku Kusi, anyamata ndi okalamba. Iwo adzakhala amaliseche ndi
opanda nsapato, matako ali pa mtunda. Zimenezi zidzachititsa manyazi
Igupto. 5 Amene ankadalira Kusi, ndiponso amene ankadzitukumula
chifukwa cha Igupto adzakhumudwa ndi kuchita manyazi. 6 Tsiku
limenelo anthu amene amakhala m'mbali mwa nyanja adzati, 'Taonani
zomwe zawachitikira amene ife tinkawadalira, amene ife tinkathawirako
kuti atithandize ndi kutipulumutsa kwa mfumu ya ku Asiriya! Nanga ife
tidzapulumuka bwanji?' "

# 21

*Za Chilango cha Babuloni*

1 Uthenga wonena za chipululu cha m'mbali mwa Nyanja.
Ankhondo a ku Elamu ndi Mediya adzabwera ngati kamvuluvulu amene
akuwomba modutsa m'mbali ya nyanja,
kuchokera ku chipululu,
dziko lochititsa mantha.

2 Ine ndaona zinthu zoopsa m'masomphenya:
Wonyenga akunyenga, wofunkha akufunkha komanso owononga
akuwononga.
Elamu, yambani nkhondo! Mediya, zingani mzinda!
Ine ndidzathetsa mavuto onse amene anayambitsa Ababuloni.

3 Chifukwa cha zimenezi thupi langa likunjenjemera ndi mantha,
ndikumva ululu ngati wa mayi amene akubereka;
ndikuvutika kwambiri ndi zimene ndikumva,
ndathedwa nzeru ndi zimene ndikuziona.
4 Mtima wanga ukugunda,
ndipo ndikunjenjemera ndi mantha;
chisisira chimene ndakhala ndikuchifuna
chasanduka chinthu choopsa kwa ine.

5 Ankhondo a ku Elamu ndi Mediya akukonza matebulo,
akuyala mphasa,
akudya komanso kumwa!
Mwadzidzidzi anamva mawu akuti, "Dzukani inu ankhondo,
pakani mafuta zishango zanu!"
6 Zimene Ambuye akunena kwa ine ndi izi;
"Pita, kayike mlonda
kuti azinena zimene akuziona.
7 Taonani, anthu akubwera ali pa akavalo
ndipo akuyenda awiriawiri,
okwera pa bulu
kapena okwera pa ngamira,
mlondayo akhale tcheru kwambiri."
8 Ndipo mlondayo anafuwula kuti,
"Ambuye anga, tsiku ndi tsiku ndimakhala pa nsanja yolondera;
Usiku uliwonse ndimakhala pa malo anga olondera.
9 Taonani, uyo munthu akubwera atakwera pa galeta
ali ndi gulu la akavalo.

Mmodzi wa iwo akuti,
‘Babuloni wagwa, wagwa!
Mafano onse a milungu yake
agwa pansi ndipo aphwanyika!’ ”

10 Inu anthu anga opunthidwa ndi kupetedwa ngati tirigu,
ine ndikukuwuzani zimene ndamva
ndikukuwuzani Uthenga wochokera kwa Yehova Wamphamvuzonse,
Mulungu wa Israeli.

*Za Chilango cha Edomu*

11 Uthenga wonena za Duma:
Munthu wina akundiyitana kuchokera ku Seiri kuti,
“Iwe mlonda, usikuwu utha liti?
Iwe mlonda, utha liti kodi usikuwu?”
12 Mlonda akuyankha kuti,
“Kukucha, koma kudanso.
Ngati ukufuna kufunsa, funsa tsopano;
ndipo ubwerenso udzafunse.”

*Za Chilango cha Arabiya*

13 Uthenga wonena za Arabiya:
Inu anthu amalonda a ku Dedani,
amene usiku mumagona m’zithukuluzi za ku Arabiya,
14 perekani madzi kwa anthu aludzu.
Inu anthu a ku Tema
perekani chakudya kwa anthu othawa nkhondo.
15 Iwo akuthawa malupanga,
lupanga losololedwa,
akuthawa uta wokokakoka
ndiponso nkhondo yoopsa.
16 Zimene Ambuye akunena kwa ine ndi izi: “Chaka chimodzi
chisanathe, potsata mmene amawerengera munthu waganyu, ulemerero
wonse wa Kedara udzatheratu. 17 Mwa anthu okoka uta, ankhondo a
ku Kedara opulumuka adzakhala owerengeka.” Wayankhula ndi Yehova
Mulungu wa Israeli.

# 22

*Za Chilango cha Yerusalemu*

1 Uthenga wonena za Chigwa cha Masomphenya:
Kodi chachitika n’chiyani,
kuti nonsenu mukwere pa madenga?
2 Iwe mzinda wodzaza ndi chisangalalo chodzaza tsaya,
iwe mzinda waphokoso ndi wosokonekera?
Anthu ako ophedwa aja sanaphedwe ndi lupanga,
kapena kufera pa nkhondo.
3 Atsogoleri ako onse ngakhale anathawa limodzi;
koma anagwidwa osadziteteza n’komwe.
Inu munapezeka ndipo nonse pamodzi munatengedwa ukapolo,
ngakhale munathawa pamene mdani akanali patali.
4 N’chifukwa chake Ine ndinati, “Chokani pamaso panga;
ndilekeni ndilire ndi mtima wowawa.
Musayesere kunditonthoza

chifukwa cha kuwonongeka kwa anthu anga.”

5 Lero Ambuye Yehova Wamphamvuzonse walola kuti tione
mavuto ndi kugonjetsedwa ndiponso chisokonezo
m’Chigwa cha Masomphenya.
Malinga agumuka,
komanso anthu akanalira mofuwula ku mapiri.
6 Ankhondo a ku Elamu anadza pa magaleta
ndi akavalo ali ndi mivi m’manja.
Ankhondo a ku Kiri anakonzeka ndi zishango.
7 Zigwa zanu zachonde ndi zodzaza ndi magaleta,
ndipo asilikali okwera pa akavalo ayikidwa pa zipata za mzinda;
8 zonse zoteteza Yuda zachotsedwa.

Ndipo tsiku limenelo munayang’anayang’ana
zida zankhondo zomwe zinali m’nyumba yaufumu ya nkhalango;
9 inu munaona kuti makoma ambiri a mzinda wa Davide
anali ndi malo ambiri ogumuka;
munasunga madzi
mu chidziwe chakumunsi.
10 Munawerenga nyumba zonse za mu Yerusalemu
ndipo munagwetsa nyumba zina kuti mulimbitse linga logumuka lija.
11 Pakati pa makoma awiri munamanga chitsime
chosungiramo madzi ochokera ku dziwe lakale,
koma inu simunadalire Mulungu amene anapanga zimenezi,
kapena kusamalako za Iye amene anazilenga kale lomwe.

12 Pa tsiku limenelo, Ambuye Yehova Wamphamvuzonse
anakuyitananani kuti mulire ndi kukhetsa misozi;
kumeta mutu wanu mpala
ndi kuvala ziguduli.
13 Koma m’malo mwake inu munakondwa ndi kusangalala;
munapha ng’ombe ndi nkhosa;
munadya nyama ndi kumwa vinyo.
Inu mumati, “Tiyeni tidye ndi kumwa
pakuti mawa tifa!”
14 Yehova Wamphamvuzonse wandiwululira mondinong’oneza kuti,
“Tchimo limeneli sindidzakhululuka mpaka tsiku la kufa kwanu,” akutero
Ambuye, Yehova Wamphamvuzonse.
15 Chimene Ambuye, Yehova Wamphamvuzonse akuti,
“Pita, ukanene kwa Sabina kapitawo,
amene amayang’anira nyumba yaufumu:
16 Kodi ukuchita chiyani kuno, nanga ndani anakupatsa chilolezo
kuti udzikumbire manda kuno,
kudzikumbira manda pa phiri
ndi kudzisemera malo opumulira m’thanthwe?

17 “Samalira, Yehova watsala pang’ono kukugwira zolimba
ndi kukuponya mwamphamvu, iwe munthu wamphamvu.
18 Iye adzakukulunga kwambiri ngati mpira
ndipo adzakuponyera m’dziko lalikulu.
Kumeneko ndiko ukafere

ndipo kumeneko ndiko kudzatsalire magaleta ako.
Ndipo udzasanduka wochititsa manyazi nyumba ya mbuye wako.
19 Ine ndidzakuchotsa pa ukapitawo wako
ndipo ndidzakutsitsa pa udindo wako.
20 “Tsiku limenelo ndidzayitanitsa mtumiki wanga, Eliyakimu mwana
wa Hilikiya. 21 Ndidzamuveka mkanjo wako ndi kumangira lamba
wako m'chiwuno mwake ndi kumupatsa ulamuliro wako. Iye adzakhala
kholo la amene amakhala mu Yerusalemu ndiponso a fuko la Yuda.
22 Ndidzamupatsa ulamuliro wa banja la Davide. Adzatsekula ndipo
palibe adzatseke, adzatseka popanda wina kutsekula. 23 Ufumu wake
udzakhala wokhazikika ngati chikhomo chokhomedwa pa malo olimba.
Anthu adzalemekeza nyumba ya abale ake chifukwa cha iye. 24 Ana ndi
abale a nyumba ya abambo ake adzakhala ngati katundu pa iye ngati
ziwiya zopanda ntchito zimene zapachikidwa pa chikhomo.
25 “Yehova Wamphamvuzonse akunena kuti, ‘Tsiku limeneli chikhomo
chokhomedwa kwambiri chija sichidzalimbanso; chidzazuka ndipo
chidzagwa ndipo zonse zopachikidwa zidzawonongedwa.’ ” Yehova
wayankhula chomwechi.

# 23

*Za Chilango cha Turo*

1 Uthenga wonena za Turo:
Lirani mofuwula, inu oyendetsa sitima za pa madzi za ku Tarisisi:
pakuti mzinda wa Turo wawonongedwa
ndipo mulibe nyumba kapena dooko.
Zimenezi anazimva
pochokera ku Kitimu.

2 Khalani chete inu anthu okhala m'mbali mwa nyanja,
inu amalonda a ku Sidoni,
iwe amene unalemera ndi anthu oyenda pa nyanja.
3 Pa nyanja zazikulu
panabwera tirigu wa ku Sihori;
zokolola za ku Nailo, ndipo munachita malonda
ndi anthu a mitundu ina.

4 Chita manyazi, iwe Sidimu
pakuti nyanja yayankhula, linga la ku nyanja (Turo) layankhula kuti,
“Sindinamvepo zowawa za kubereka kapena kuberekapo mwana;
sindinalerepo ana aamuna kapena kulera ana aakazi.”
5 Mawuwa akadzamveka ku Igupto,
iwo adzachita mantha akadzamva kuti Turo wawonongeka.

6 Wolokerani ku Tarisisi,
lirani mofuwula, inu anthu okhala m'mbali mwa nyanja.
7 Kodi uwu si mzinda wachisangalalo uja,
mzinda wakalekale,
umene anthu ake ankapita
kukakhala ku mayiko akutali?
8 Kodi ndani anakonza zimenezi kuti zigwere Turo, mzinda umene
unakhazikitsa mizinda ina,
mzinda umene amalonda ake ndi akalonga

ndi otchuka
pa dziko lapansi?
9 Yehova Wamphamvuzonse anakonza zimenezi
kuti athetse kunyada kwawo
ndi kutsitsa anthu otchuka a pa dziko lapansi.

10 Mubalalike m'dziko mwanu ngati mtsinje wa Nailo
inu anthu a ku Tarisisi,
pakuti mulibenso chokutetezani.
11 Yehova watambasula dzanja lake kuloza ku nyanja
ndipo wagwedeza maufumu ake.
Iye walamula kuti Kanaani
agwetse malinga ake.
12 Iye anati, "Simudzakondwanso konse,
inu anthu opanikizidwa a ku Sidoni, tsopano wamphwanyidwa!

"Ngakhale muwolokere ku Kitimu,
kumeneko simukapezako mpumulo."
13 Onani dziko la Ababuloni,
anthu amenewa tsopano atheratu!
Asiriya asandutsa Turo kukhala
malo a zirombo za ku chipululu;
anamanga nsanja zawo za nkhondo,
anagumula malinga ake
ndipo anawasandutsa bwinja.

14 Lirani mofuwula, inu anthu oyendetsa sitima za pa madzi za ku Tarisisi;
chifukwa malinga ako agwetsedwa!
15 Pa nthawi imeneyo Turo adzayiwalika pa zaka 70, amene ndi masiku
a moyo wa mfumu. Koma potsiriza pa zaka 70 zimenezi, Turo adzakhala
ngati mkazi wachiwerewere woyimbidwa mu nyimbo:
16 "Tenga zeze wako uzungulire mzinda,
iwe mkazi wachiwerewere woyiwalika;
imba zeze mokometsera, imba nyimbo zambiri,
kuti anthu akukumbukire."
17 Pakutha pa zaka 70, Yehova adzachitapo kanthu pa Turo. Iye
adzabwerera ku ntchito yake yakale monga mkazi wachiwerewere ndipo
adzachita zachiwerewere ndi maufumu onse a dziko lapansi. 18 Koma
phindu lake ndi malipiro ake adzazipereka kwa Yehova; sadzazikundika
kapena kuzisunga. Phindu lake lidzapita kwa mtumiki wa Yehova kuti
agule zakudya zambiri ndi zovala zokongola.

# 24

*Chilango cha Yehova pa Dziko Lapansi*

1 Taonani, Yehova adzawononga dziko lapansi
ndi kulisandutsa chipululu;
Iye adzasakaza maonekedwe ake
ndi kumwaza anthu ake onse.
2 Aliyense zidzamuchitikira mofanana:
wansembe chimodzimodzi munthu wamba,
antchito aamuna mofanananso ndi ambuye awo aamuna,
antchito aakazi chimodzimodzi ambuye awo aakazi,

wogula chimodzimodzi wogulitsa,
wobwereka chimodzimodzi wobwereketsa,
okongola chimodzimodzi okongoza.
3 Dziko lapansi lidzawonongedwa kwathunthu
ndi kusakazikiratu.
Yehova wanena mawu awa.

4 Dziko lapansi likulira ndipo likufota,
dziko lonse likuvutika ndipo likuwuma,
anthu omveka a dziko lapansi akuvutika.
5 Anthu ayipitsa dziko lapansi;
posamvera malangizo ake;
pophwanya mawu ake
ndi pangano lake lamuyaya.
6 N'chifukwa chake matemberero akuwononga dziko lapansi;
anthu a m'dzikomo akuzunzika chifukwa cha kulakwa kwawo,
iwo asakazika
ndipo atsala ochepa okha.
7 Vinyo watsopano watha ndipo mphesa zikufota;
onse okonda zosangalatsa ali ndi chisoni.
8 Kulira kokometsera kwa matambolini kwatha,
phokoso la anthu osangalala latha,
zeze wosangalatsa wati zii.
9 Anthu sadzayimbanso akumwa vinyo;
akadzamwa zaukali zidzakhala zowawa m'kamwa mwawo.
10 Mzinda wachisokonezo uja wawonongeka;
nyumba iliyonse yatsekedwa.
11 Anthu akulira m'misewu kufuna vinyo;
chimwemwe chonse chatheratu,
palibenso chisangalalo pa dziko lapansi.
12 Mzinda wasanduka bwinja
zipata zake zagumuka.
13 Zimenezi ndizo zidzachitikire mitundu yonse ya dziko lapansi
ndiponso pakati pa mitundu ya anthu.
Zidzakhala ngati pamene mitengo ya olivi yayoyoledwa,
kapena ngati nthawi ya kunkha la mphesa atatsiriza kukolola.

14 Koma otsala onse akufuwula ndi kuyimba mwachimwemwe;
anthu akumadzulo akutamanda ukulu wa Yehova.
15 N'chifukwa chake inu akummawa, tamandani Yehova;
ndi inu okhala m'mphepete mwa nyanja kwezani dzina la Yehova,
Mulungu wa Israeli.
16 Kuchokera kumalekezero a dziko lapansi tikumva kuyimba kotamanda
"Wolungamayo."

Koma ine ndinati, "Ndatheratu, ndatheratu!
Tsoka kwa ine!
Anthu achinyengo akupitirizabe kuchita zachinyengo,
inde chinyengo chawo chikunkerankera m'tsogolo."
17 Inu anthu adziko lapansi, zoopsa, dzenje
ndi msampha zikukudikirani.
18 Aliyense wothawa phokoso la zoopsa
adzagwa m'dzenje;

ndipo aliyense wotuluka m'dzenjemo
adzakodwa ndi msampha.

Zitseko zakumwamba zatsekulidwa,
ndipo maziko a dziko lapansi agwedezeka.
19 Dziko lapansi lathyokathyoka,
ndipo lagawika pakati,
dziko lapansi lagwedezeka kotheratu.
20 Dziko lapansi likudzandira ngati munthu woledzera
likugwedezeka ndi mphepo ngati chisimba;
lalemedwa ndi machimo ake.
Lidzagwa ndipo silidzadzukanso.

21 Tsiku limenelo Yehova adzalanga
amphamvu a kumwamba
ndiponso mafumu apansi pano.
22 Mulungu adzawasonkhanitsa pamodzi
ngati am'ndende amene ali m'dzenje.
Adzawatsekera m'ndende
ndipo adzalangidwa patapita nthawi yayitali.
23 Mwezi udzanyazitsidwa, dzuwa lidzachita manyazi;
pakuti Yehova Wamphamvuzonse adzakhala mfumu ndipo adzalamulira;
pa Phiri la Ziyoni ndi ku Yerusalemu,
ndipo adzaonetsa ulemerero wake pamaso pa akuluakulu.

# 25

*Nyimbo Yotamanda Yehova*

1 Yehova ndinu Mulungu wanga;
ine ndidzakukwezani ndi kutamanda dzina lanu,
pakuti mwachita zodabwitsa
zimene munakonzekeratu kalekale
mokhulupirika kwambiri.
2 Inu mwasandutsa mzinda uja kukhala mulu wamiyala.
Ndipo mzinda wamalinga wasanduka bwinja,
linga la anthu achilendo lero si mzindanso
ndipo sidzamangidwanso.
3 N'chifukwa chake anthu amphamvu adzakulemekezani;
mizinda ya mitundu ya anthu ankhanza idzakuopani.
4 Inu mwakhala ngati populumukira pa anthu osauka,
mwakhala ngati kobisalirako munthu wovutika pa nthawi ya masautso ake.
Mwakhala ngati pobisalirapo
pa nthawi ya mphepo yamkuntho ndi mthunzi pa nthawi ya dzuwa.
Pakuti anthu ankhanza
ali ngati mphepo yamkuntho yowomba pa khoma,
5 ndiponso ngati kutentha m'dziko lowuma.
Inu mumaletsa phokoso la anthu achilendo.
Monga momwe mthunzi wa mtambo umachepetsa kutentha,
inu munaletsa nyimbo za anthu ankhanza.

6 Pa phiri ili Yehova Wamphamvuzonse adzakonzera

anthu a mitundu yonse madyerero a zakudya zokoma ndi vinyo wabwino.
Phwando la nyama yonona
ndi vinyo wabwino kwambiri.
7 Iye adzachotsa kulira
kumene kwaphimba anthu ngati nsalu.
Adzachotsa chinsalu chimene chakuta mitundu yonse ya anthu.
8 Yehova adzathetsa imfa mpaka muyaya,
Ambuye Yehova adzapukuta misozi m'maso
mwa munthu aliyense;
adzachotsa manyazi a anthu ake
pa dziko lonse lapansi,
Yehova wayankhula.
9 Tsiku limenelo iwo adzati,
"Ndithudi, uyu ndiye Mulungu wathu;
ife tinamudalira ndipo anatipulumutsa.
Uyu ndiye Yehova, ife tinamudalira;
tiyeni tikondwe ndi kusangalala chifukwa watipulumutsa."

10 Yehova adzateteza phiri limeneli ndi dzanja lake;
ndipo Amowabu adzawapondereza pomwe alilipo,
ngati mmene amapondera manyowa m'dzenje.
11 Amowabuwo adzatambasula manja awo m'menemo,
ngati mmene amachitira munthu wosambira.
Koma Mulungu adzathetsa kunyada kwawo
ngakhale luso la manja awo.
12 Iye adzagumula malinga awo ataliatali
ndipo adzawagwetsa
ndi kuwaponya pansi,
pa fumbi penipeni.

# 26

*Nyimbo ya Matamando*

1 Tsiku limenelo anthu a m'dziko la Yuda adzayimba nyimbo iyi.
Tili ndi mzinda wolimba.
Mulungu amawuteteza ndi zipupa
ndi malinga.
2 Tsekulani zipata za mzinda
kuti mtundu wolungama
ndi wokhulupirika ulowemo.
3 Inu mudzamupatsa munthu
wa mtima wokhazikika
mtendere weniweni.
4 Mudalireni Yehova mpaka muyaya,
chifukwa Yehova Mulungu ndiye Thanthwe losatha.
5 Iye amatsitsa anthu amene amadziyika pamwamba,
iye amagwetsa pansi mzinda wodzitukumula,
amagumula makoma ake
ndi kuwagwetsa pansi pa fumbi penipeni.
6 Mapazi a anthu akuwupondereza,
mapazi a anthu oponderezedwa,
mapazi anthu osauka.

7 Njira ya munthu wolungama ndi yosalaza,
Inu Wolungamayo, mumasalaza njira ya wolungama.
8 Inde Yehova, timayenda m'njira zanu zolungama,
ife timayembekezera Inu;
mitima yathu imakhumba kukumbukira
ndi kulemekeza dzina lanu.
9 Moyo wanga umalakalaka Inu usiku wonse;
nthawi yammawa ndimafunafuna Inu.
Pamene muweruza dziko lapansi
anthu amaphunzira kuchita chilungamo.
10 Ngakhale mukomere mtima anthu oyipa,
saphunzira chilungamo.
Amachita zoyipa m'dziko la chilungamo,
ndipo sazindikira ululu wa Yehova.
11 Inu Yehova, mwatukula dzanja lanu kuti muwalange,
koma iwo sakuliona dzanjalo.
Aloleni anthu aone ndi kuchita manyazi poona mmene mukondera anthu anu;
ndipo moto umene mwasonkhera adani anu uwapsereze.

12 Yehova, mumatipatsa mtendere;
ndipo zonse zimene ife tinazichita munatichitira ndinu.
13 Inu Yehova Mulungu wathu, ngakhale takhala tikulamulidwa ndi ena m'malo mwanu,
koma ife timalemekeza dzina lanu lokha.
14 Iwo tsopano sadzadzukanso;
mizimu yawo sidzabwera kudzativutitsa
pakuti mwawalanga ndipo mwawawononga;
palibenso amene amawakumbukira.
15 Inu Yehova, mwaukulitsa mtundu wathu;
mwauchulukitsa ndithu
ndipo mwalandirapo ulemu;
mwaukuza mbali zonse za dziko.

16 Yehova, anthu anu anabwera kwa Inu pamene anali m'masautso;
pamene munawalanga,
iwo anapemphera kwa Inu.
17 Monga mayi woyembekezera pamene nthawi yake yobereka yayandikira
amamva kupweteka ndipo amalira ndi ululu,
ifenso tinali chimodzimodzi pamaso panu, Inu Yehova.
18 Ife chimodzimodzi tinamva ululu, ngati mayi pa nthawi yobala mwana,
koma sitinapindulepo kanthu,
kapena kupulumutsa dziko lapansi;
sitinabadwitse anthu atsopano pa dziko pano.

19 Koma anthu anu amene anafa adzakhalanso ndi moyo;
matupi awo adzadzuka.
Iwo amene ali ku fumbi tsopano
adzadzuka ndi kuyimba mosangalala.
Monga mame amafewetsa pansi kutsitsimutsa zomera,
momwenso Yehova adzaukitsa anthu amene anafa kale.

20 Abale anga, pitani mukalowe m'nyumba zanu
ndipo mukadzitsekere;
mukabisale kwa kanthawi kochepa
mpaka ukali wake utatha.
21 Taonani, Yehova akubwera kuchokera kumene amakhala;
akubwera kudzalanga anthu a dziko lapansi chifukwa cha machimo awo.
Dziko lapansi lidzawulula magazi amene anakhetsedwa pa dzikolo;
dziko lapansi silidzabisanso mitembo ya anthu ophedwa.

# 27

*Za Munda Wamphesa wa Yehova*

1 Tsiku limenelo,
Yehova ndi lupanga lake
lakuthwa, lalikulu ndi lamphamvu,
adzalanga Leviyatani chinjoka chothawa chija,
Leviyatani chinjoka chodzikulunga;
adzapha chirombo choopsa cha m'nyanja.
2 Tsiku limenelo Yehova adzati,
"Tidzayimba nyimbo ya munda wamphesa wobereka bwino:
3 Ine, Yehova, ndimawuyang'anira;
ndimawuthirira nthawi zonse.
Ndimawulondera usana ndi usiku
kuti wina angawononge.
4 Ine sindinakwiye.
Ngati mkandankhuku ndi minga zikanaoneka ndikanalimbana nazo!
Ndikachita nazo nkhondo;
ndikanazitentha zonse ndi moto.
5 Koma ngati apo ayi, abweretu kwa Ine adani angawo kuti ndidzawateteze;
apangane nane za mtendere,
indithu, apangane nane za mtendere."

6 Masiku akubwerawo Yakobo adzazika mizu,
Israeli adzaphukira ndi kuchita maluwa,
ndipo adzadzaza dziko lonse lapansi ndi zipatso.

7 Kodi Yehova anakantha Israeli
ngati momwe anakanthira anthu amene anazunza Israeli?
Kapena kodi Yehova anapha Israeli
ngati mmene anthu ena anaphera Israeli?
8 Yehova mwawalanga powapirikitsa ndi kuwatumiza ku ukapolo,
mwawachotsa ndi mpweya wanu woopsa,
monga zimachitikira pa tsiku la mkuntho wochokera kummawa.
9 Yehova adzakhululuka kulakwa kwa Yakobo.
Iwo adzaonetsa kuti alapadi pamene adzaphwanya miyala yonse ya guwa lachikunja,
ngati mmene anthu amaphwanyira miyala yanjereza
mpaka kukhala ngati fumbi lokhalokha.
Sipadzapezekanso mafano a Asera
kapena maguwa ofukiza lubani.
10 Mzinda wamalinga uja wasanduka bwinja,

wasanduka malo osiyidwa, ndi kutayidwa ngati chipululu;
kumeneko amadyetselako ana ang'ombe
kumeneko zimapumulako ziweto
ndi kumwetula nthambi za mitengo kotheratu.
11 Pamene nthambi za mitengoyo zauma, zimathyoka
ndipo amayi amabwera nazitola ndi kuzisandutsa nkhuni.
Pakuti awa ndi anthu opanda nzeru;
kotero Mulungu amene anawapanga sadzachitira chisoni,
ndipo Mlengi wawo sawakomera mtima.
12 Tsiku limenelo Yehova adzasonkhanitsa pamodzi anthu ake mmodz-
immodzi kumalo opunthira tirigu, kuchokera ku mtsinje wa Yufurate
mpaka ku mtsinje wa ku Igupto. 13 Ndipo tsiku limenelo lipenga lalikulu
lidzalira. Amene akuzunzika ku Asiriya iwo amene ali ku ukapolo
ku Igupto adzabwera ndi kudzalambira Yehova pa phiri lopatulika mu
Yerusalemu.

# 28

*Tsoka kwa Efereimu*

1 Tsoka ufumu wonyada wa zidakwa za ku Efereimu.
Tsoka kwa ulemerero wake wokongola umene ukufota ngati duwa
limene lili pa mutu pa anthu
oledzera a m'chigwa chachonde.
2 Taonani, ambuye ali naye wina wamphamvu ndi nyonga.
Iye adzabwera ngati mkuntho wamatalala ndi namondwe
wowononga,
ngati madzi amphamvu osefukira a mvula yamkuntho;
ndipo adzawagwetsa pansi mwankhanza.
3 Ulamuliro wa atsogoleri oledzera
a ku Efereimu adzawuthetsa.
4 Ndipo ulemerero wokongola wa mzinda umene uli ngati duwa
lofota pamutu pa anthu oledzera a m'chigwa chachonde uja,
udzakhala ngati nkhuyu yoyambirira kupsa
imene munthu akangoyiona amayithyola
nthawi yokolola isanakwane.

5 Tsiku limenelo Yehova Wamphamvuzonse
adzakhala ngati nkhata yaufumu,
chipewa chokongola
kwa anthu ake otsala.
6 Iye adzapereka mtima
wachilungamo kwa oweruza,
adzakhala chilimbikitso kwa
amene amabweza adani pa zipata za mzinda.

7 Nawonso awa ali dzandidzandi chifukwa cha vinyo
ndipo akusochera chifukwa cha mowa:
ansembe ndi aneneri akudzandira chifukwa cha mowa
ndipo akusokonezeka chifukwa cha vinyo;
akusochera chifukwa cha mowa,
akudzandira pamene akuona masomphenya,
kupunthwa pamene akupereka chigamulo.
8 Pa matebulo onse pali masanzi okhaokha

ndipo palibenso malo wopanda zonyansa.

9 Iwo akuti, “Kodi munthu ameneyu akufuna aphunzitse ndani?
Uthengawu akufuna kufotokozera yani?
Ndi kwa ana amene aleka kuyamwa,
kwa makanda ongowachotsa kumene ku bere?
10 Akuyesa kumatiphunzitsa pang’onopang’ono
lemba ndi lemba, mzere ndi mzere,
phunziro ndi phunziro.
Zonsezi akungoti apa pang’ono apa pang’ono.”

11 Mulungu adzayankhula kwa anthu ake kudzera mwa anthu aziyankhulo zachilendo, ziyankhulo zosamveka bwino.
Mulungu adzayankhula kwa anthu awa, amene
12 anakuwuzani kuti,
“Malo opumulira ndi ano,
otopa apumule, malo owusira ndi ano.”
Koma inu simunamvere.
13 Choncho Yehova adzakuphunzitsani
pang’onopang’ono lemba ndi lemba,
mzere ndi mzere, phunziro ndi phunziro.
Kotero mudzayenda ndi kugwa chambuyo,
adzapweteka ndi kukodwa mu msampha
ndipo adzakutengani ku ukapolo.

14 N’chifukwa chake imvani mawu a Yehova,
inu anthu achipongwe amene mumalamulira anthu awa mu Yerusalemu.
15 Inu mumayankhula monyada kuti, “Ife tinachita pangano ndi imfa,
ife tachita mgwirizano ndi manda.
Pamene mliri woopsa ukadzafika
sudzatikhudza ife,
chifukwa timadalira bodza ngati pothawirapo pathu
ndi chinyengo ngati malo anthu obisalapo.”
16 Tsono zimene Ambuye Yehova akunena ndi izi:
“Taonani, ndikuyika mwala wovomerezeka ndi amisiri
ngati maziko mu Ziyoni,
mwala wapangodya, wamtengowapatali wopanga maziko amphamvu;
munthu amene awukhulupirira sadzagwedezeka.
17 Ntchito zolungama zidzakhala ngati chingwe choyezera maziko ake,
ndipo chilungamo chidzakhala chowongolera mzere;
matalala adzawononga malo anu othawirapo, amene ndi mabodza,
ndipo madzi adzamiza malo anu obisalako.
18 Pangano limene munachita ndi imfa lidzathetsedwa;
mgwirizano wanu ndi manda udzachotsedwa.
Pakuti mliri woopsa udzafika,
ndipo udzakugonjetsani.
19 Ndipo ukadzangofika udzakutengani.
Udzafika mmawa uliwonse,
usiku ndi usana.”

Anthu akadzamvetsetsa uthenga umenewu
adzaopsedwa kwambiri.

20 Mudzakhala ngati munthu wogona pa bedi lalifupi kwambiri kuti sangathe kutambalitsapo miyendo;
ndiponso mudzakhala ngati munthu amene wafunda bulangeti lochepa kwambiri kuti sangathe n'kufunda komwe.
21 Yehova adzamenya nkhondo monga anachitira ku phiri la Perazimu
adzakalipa monga anachitira ku chigwa cha Gibiyoni;
adzagwira ntchito yake yooneka ngati yachilendo,
ndipo zimene ati adzachite zidzakhala ngati zodabwitsa.
22 Tsopano lekani kunyoza,
mukapanda kutero maunyolo anu adzakuthinani kwambiri;
Ambuye, Yehova Wamphamvuzonse wandiwuza kuti,
"Ndagamula kuti ndidzawononga dziko lapansi."

23 Tcherani khutu ndipo mumve mawu anga;
mvetserani ndipo mumve zimene ndikunena.
24 Kodi mlimi wofuna kudzala mbewu amangokhalira kutipula kokhakokha?
Kodi amangokhalira kugawula ndi kugalawuza kokhakokha?
25 Pamene iye wasalaza mundawo,
kodi samafesa mawere ndi chitowe?
Kodi suja samadzala tirigu
ndi barele m'mizere yake,
nadzala mchewere m'phepete mwa mundawo?
26 Mulungu wake amamulangiza
ndi kumuphunzitsa njira yabwino.

27 Mawere sapunthira chopunthira cha galeta lopanda mikombero,
kapena chitowe sapuntha popondetsapo mikombero ya galeta;
mawere amapuntha ndi ndodo
ndipo chitowe amapuntha ndi kamtengo.
28 Tirigu ayenera kusinjidwa kuti apangire buledi,
komabe munthu samangokhalira kupuntha tiriguyo osalekeza, kuopa kuti angatekedzeke.
Ngakhale kuti amapuntha tiriguyo poyendetsapo mikombero ya galeta,
koma akavalo ake satekedza tiriguyo.
29 Izinso zimachokera kwa Yehova Wamphamvuzonse,
wa uphungu wodabwitsa ndi wa nzeru zopambana.

# 29

*Tsoka kwa Mzinda wa Davide*

1 Tsoka kwa iwe, Arieli, Arieli,
mzinda umene Davide anakhazikitsamo zithando za nkhondo!
Papite chaka chimodzi kapena ziwiri
ndipo masiku a zikondwerero zanu azipitirirabe ndithu.
2 Komatu Ine ndidzathira nkhondo Arieli
ndipo kudzakhala kulira ndi kudandaula,
mzindawo udzasanduka ngati ng'anjo ya guwa lansembe.
3 Ine ndidzamanga misasa ya nkhondo kulimbana ndi mzindawo;
ndidzakuzungulira ndi nsanja za nkhondo
ndi kumanga mitumbira yanga ya nkhondo kulimbana nawe.
4 Utagwetsedwa pansi, iwe udzayankhula kuchokera m'nthaka,
mawu ako adzatuluka uli m'fumbi,

adzamveka ngati a mzukwa.
Mawu ako adzamveka ngati onong'ona kuchokera m'fumbi.

5 Koma chigulu cha adani ako chidzasanduka chifwirimbwiti.
Chigulu cha ankhondo achilendo chidzabalalika ngati mungu wowuluzika ndi mphepo.
Mwadzidzidzi ndi mosayembekezereka,
6 Yehova Wamphamvuzonse adzabwera
ndi mabingu ndi chivomerezi ndi phokoso lalikulu,
kamvuluvulu ndi namondwe ndi malawi a moto wonyeketsa.
7 Tsono chigulu chankhondo cha mitundu ina yonse chimene chikulimbana ndi mzinda wa Arieli
n'kumathira nkhondo mzindawo, malinga ake ndi kuwuzinga,
chigulu chonsecho chidzazimirira ngati maloto,
gati zinthu zoziona m'masomphenya usiku.
8 Chidzakhala ngati munthu wanjala wolota akudya,
koma podzuka ali nayobe njala;
kapena ngati munthu waludzu wolota akumwa,
koma podzuka, ali nalobe ludzu, kummero kwake kuli gwaa.
Izi zidzachitika pamene chigulu cha nkhondo cha mitundu ina yonse
chikunthira nkhondo Phiri la Ziyoni.

9 Pitirizani kuledzera ndipo mudzakhala opusa.
Dzitsekeni m'maso ndipo mukhale osapenya,
ledzerani, koma osati ndi vinyo,
dzandirani, koma osati ndi mowa.
10 Yehova wakugonetsani tulo tofa nato.
Watseka maso anu, inu aneneri;
waphimba mitu yanu, inu alosi.
11 Kwa inu mawu onsewa ali ngati buku lotsekedwa, ndipo ngati
lipatsidwa kwa wina wodziwa kuwerenga ndi kunena kuti, "Chonde
tawerengani bukuli," iye adzati, "Sindingathe popeza ndi lomatidwa."
12 Kapena ngati lipatsidwa kwa amene sadziwa kuwerenga ndi kunena
kuti, "Chonde werenga bukuli," iye adzayankha kuti, "Ine sindidziwa
kuwerenga."
13 Ambuye akuti,
"Anthu awa amandipembedza Ine ndi pakamwa pawo,
ndi kundilemekeza Ine ndi milomo yawo,
koma mitima yawo ili kutali ndi Ine.
Kundipembedza kwawo ndi kwa chiphamaso.
Amandipembedza motsata malamulo a anthu amene anaphunzitsidwa.
14 N'chifukwa chakenso Ine ndidzapitirira
kuwachitira ntchito zodabwitsa;
nzeru za anthu anzeru zidzatha,
luntha la anthu aluntha Ine ndidzalinyoza."
15 Tsoka kwa amene amayesetsa
kubisira Yehova maganizo awo,
amene amachita ntchito zawo mu mdima n'kumanena kuti,
"Ndani amene akundiona kapena ndani akudziwa zimene ndikuchita?"
16 Inu mumazondotsa zinthu
ngati kuti dothi lasanduka wowumba mbiya.

Kodi chinthu chopangidwa chingawuze wochipanga kuti
"Sunandipange ndi iwe?"
Kapena m'phika kunena kwa amene anawuwumba kuti,
"Iwe sudziwa chilichonse?"

17 Kodi Lebanoni posachedwapa sadzasanduka munda wachonde,
ndipo kodi munda wachondewo ngati nkhalango?
18 Tsiku limenelo anthu osamva adzamva mawu a m'buku,
ndipo anthu osaona amene
ankakhala mu mdima adzapenya.
19 Anthu odzichepetsa adzakhalanso ndi chimwemwe mwa Yehova;
ndipo anthu osowa adzakondwa chifukwa cha Woyerayo wa Israeli.
20 Koma anthu ankhanza adzazimirira,
oseka anzawo sadzaonekanso,
ndipo onse okopeka ndi zoyipa adzawonongedwa.
21 Yehova adzalanga amene amasinjirira munthu kuti apezeke wolakwa,
kapena kuphophonyetsa anthu ozenga mlandu
ndi umboni wonama kuti osalakwa asaweruzidwe mwachilungamo.
22 Choncho Yehova amene anawombola Abrahamu, akunena kwa
zidzukulu za Yakobo kuti,
"Anthu anga sadzachitanso manyazi;
nkhope zawo sizidzagwanso ndi manyazi.
23 Akadzaona ana awo ndi
ntchito ya manja anga pakati pawo,
adzatamanda dzina langa loyera;
adzazindikira kuyera kwa Woyerayo wa Yakobo,
ndipo adzachita naye mantha Mulungu wa Israeli.
24 Anthu opusa adzapeza nzeru;
onyinyirika adzalandira malangizo."

# 30

*Tsoka kwa Mtundu Wopanduka*

1 Yehova akuti, "Tsoka kwa ana ondipandukira
amene amachita zowakomera iwo okha osati Ine,
nachita mgwirizano wawowawo
koma osati motsogozedwa ndi Ine.
Choncho amanka nachimwirachimwira.
2 Amapita ku Igupto kukapempha thandizo
koma osandifunsa;
amathawira kwa Farao kuti awateteze,
ku Igupto amafuna malo opulumulira.
3 Koma chitetezo cha Farao chidzakhala manyazi anu,
malo a mthunzi a ku Igupto mudzachita nawo manyazi.
4 Ngakhale kuti nduna zawo zili ku Zowani,
ndipo akazembe awo afika kale ku Hanesi,
5 aliyense wa ku Yuda adzachita manyazi
chifukwa cha anthu opanda nawo phindu,
amene sabweretsa thandizo kapena phindu,
koma manyazi ndi mnyozo."
6 Uthenga wonena za nyama za ku Negevi:
Akazembe akuyenda m'dziko lovuta ndi losautsa,
m'mene muli mikango yayimuna ndi yayikazi,

mphiri ndi njoka zaululu.
Iwo amasenzetsa abulu ndi ngamira chuma chawo,
kupita nazo kwa mtundu wa anthu
umene sungawathandize.
7 Amapita ku Igupto amene thandizo lake ndi lachabechabe.
N’chifukwa chake dzikolo ndalitcha
Rahabe chirombo cholobodoka.

8 Yehova anandiwuza kuti, “Tsopano pita,
ukalembe zimenezi m’buku iwo akuona
ndipo lidzakhala ngati umboni wosatha
masiku a m’tsogolo.
9 Amenewa ndi anthu owukira, onama ndi
osafuna kumvera malangizo a Yehova.
10 Iwo amawuza alosi kuti,
‘Musationerenso masomphenya!’
Ndipo amanena kwa mneneri kuti,
‘Musatinenerenso zoona,’
mutiwuze zotikomera,
munenere za m’mutu mwanu.
11 Patukani pa njira ya Yehova,
lekani kutsata njira ya Yehova;
ndipo tisamvenso mawu
a Woyerayo uja wa Israeli!”
12 N’chifukwa chake Woyerayo wa Israeli akunena kuti,
“Popeza inu mwakana uthenga uwu,
mumakhulupirira zopondereza anzanu
ndipo mumadalira kuchita zoyipa,
13 choncho tchimo linalo lidzakhala ngati ming’alu
pa khoma lalitali ndi lopendama
limene linagwa mwadzidzidzi ndi mwamsangamsanga.
14 Lidzaphwanyika ngati mbiya
imene yanyenyekeratu,
mwakuti pakati pake sipadzapezeka phale ngakhale
lopalira moto m’ng’anjo
kapena lotungira madzi m’chitsime.”
15 Zimene Ambuye Yehova, Woyerayo wa Israeli ananena ndi izi:
“Ngati mubwerera ndi kupuma mudzapulumuka,
ngati mukhala chete ndi kukhulupirira mudzakhala amphamvu,
koma inu munakana zimenezi.
16 Inu mukuti, ‘Ayi ife tidzathawa,
tidzakwera pa akavalo aliwiro.’
Zoonadi kuti mudzakwera pa akavalo aliwiro,
koma okuthamangitsani adzakhalanso aliwiro.
17 Anthu 1,000 mwa inu adzathawa
poona mdani mmodzi;
poona adani asanu okha
nonsenu mudzathawa.
Otsala anu
adzakhala ngati mbendera pa phiri,
ndi ngati chizindikiro cha pa chulu.”

18 Komatu Yehova akufunitsitsa kuti akukomereni mtima,

iye ali wokonzeka kuti akuchitireni chifundo.
Pakuti Yehova ndi Mulungu wachilungamo.
Ndi odala onse amene amakhulupirira Iye!
19 Inu anthu a ku Ziyoni, amene mukhala mu Yerusalemu simudzali-
ranso. Mulungu adzakukomerani mtima pamene adzamva kulira kwanu
kopempha thandizo! Ndipo akadzamva, adzakuyankhani. 20 Ngakhale
Ambuye adzakulowetseni m'masautso, aphunzitsi anu sadzakhala kakasi;
inu mudzawaona ndi maso anuwo. 21 Ngati mudzapatukira kumanja
kapena kumanzere, mudzamva mawu kumbuyo kwanu woti, "Njira
ndi iyi; yendani m'menemo." 22 Pamenepo mudzawononga mafano
anu okutidwa ndi siliva ndiponso zifanizo zanu zokutidwa ndi golide;
mudzawataya ngati zinthu zonyansa ndipo mudzati, "Zichoke zonsezi!"
23 Yehova adzakugwetseraninso mvula pa mbewu zanu zimene
mukadzale m'nthaka, ndipo chakudya chimene mudzakolole chidzakhala
chabwino ndi chochuluka. Tsiku limenelo ng'ombe zanu zidzadya
msipu wochuluka. 24 Ng'ombe ndi abulu amene amalima m'munda
adzadya chakudya chamchere, chopetedwa ndi foloko ndi fosholo. 25 Pa
tsiku limene adani anu adzaphedwa ndi nsanja zawo kugwa, mitsinje
ya madzi idzayenda pa phiri lililonse lalikulu ndi pa phiri lililonse
laling'ono. 26 Mwezi udzawala ngati dzuwa, ndipo kuwala kwa dzuwa
kudzawonjezereka kasanu n'kawiri, ngati kuwala kwa tsiku limodzi.
Yehova adzamanga mabala a anthu ake ndi kupoletsa zilonda zimene Iye
anachititsa polanga anthu ake.

27 Taonani, Yehova akubwera kuchokera kutali,
ndipo mkwiyo wake ndiwonyeka ndi chiweruzo chake chidzakhala chopweteka.
Iye wayankhula mwaukali kwambiri,
ndipo mawu ake ali ngati moto wonyeka.
28 Mpweya wake uli ngati mtsinje wosefukira,
wa madzi ofika m'khosi.
Iye adzasefa anthu a mitundu ina ndi sefa wosakaza;
Iye akuyika zitsulo m'kamwa mwa anthu a mitundu ina ngati akavalo,
kuti ziwasocheretse.
29 Ndipo inu mudzayimba
mokondwa monga mumachitira usiku pa chikondwerero chopatulika.
Mudzasangalala
ngati anthu oyimba zitoliro
popita ku phiri la Yehova,
thanthwe la Israeli.
30 Anthu adzamva liwu la ulemerero la Yehova
ndipo adzaona dzanja lake likutsika pa iwo
ndi mkwiyo woopsa, pamodzi ndi moto wonyeketsa,
mphenzi, namondwe ndi matalala.
31 Asiriya adzaopa liwu la Yehova,
ndipo Iye adzawakantha ndi ndodo.
32 Yehova akamadzalanga adani ake ndi ndodo,
anthu ake adzakhala akuvina nyimbo
zoyimbira matambolini ndi azeze,
Yehova ndiye ati adzamenyane ndi Asiriyawo.
33 Malo otenthera zinthu akonzedwa kale;
anakonzera mfumu ya ku Asiriya.
Dzenje la motolo ndi lozama ndi lalikulu,
ndipo muli nkhuni zambiri;

mpweya wa Yehova,
wangati mtsinje wa sulufule,
udzayatsa motowo pa nkhunizo.

## 31

*Tsoka kwa Amene Amadalira Igupto*

1 Tsoka kwa amene amapita ku Igupto kukapempha chithandizo,
amene amadalira akavalo,
nakhulupirira kuchuluka kwa magaleta awo ankhondo
ndiponso mphamvu za asilikali awo okwera pa akavalo,
koma sakhulupirira Woyerayo wa Israeli,
kapena kupempha chithandizo kwa Yehova.
2 Komatu Yehovayo ndi wanzeru ndipo angathe kuwononga,
ndipo sasintha chimene wanena.
Adzalimbana ndi anthu ochita zoyipa,
komanso ndi amene amathandiza anthu ochita zoyipa.
3 Aigupto ndi anthu chabe osati Mulungu;
akavalo awo ndi nyama chabe osati mizimu.
Yehova akangotambasula dzanja lake,
amene amapereka chithandizo adzapunthwa,
amene amalandira chithandizocho adzagwa;
onsewo adzathera limodzi.
4 Zimene Yehova akunena kwa ine ndi izi:
"Monga mkango kapena msona wamkango umabangula
ukagwira nyama yake,
ndipo suopsedwa kapena kusokonezeka
ndi kufuwula kwa abusa amene akulimbana nayo,
momwemonso palibe chingaletse
Yehova Wamphamvuzonse
kubwera kudzatchinjiriza
phiri la Ziyoni ndi zitunda zake.
5 Monga mbalame zowuluka pamwamba pa zisa zake,
Yehova Wamphamvuzonse adzatchinjiriza Yerusalemu;
ndi kumupulumutsa,
iye adzawupitirira ndi kuwulanditsa."
6 Inu Aisraeli, bwererani kwa Iye amene munamuwukira kwakukulu.
7 Pakuti tsiku limenelo nonsenu mudzataya mafano anu a siliva ndi golide
amene mumapanga ndi manja anu auchimo.
8 "Aasiriya adzaphedwa ku nkhondo ndi mphamvu osati za munthu.
Lupanga, osati la munthu, lidzawawononga.
Adzathawa ku nkhondo ndipo anyamata awo
adzagwira ntchito yathangata.
9 Mfumu yawo idzamwalira ndi mantha,
ndipo atsogoleri awo ankhondo adzathawa ndi mantha
kusiya pambuyo mbendera yawo ya nkhondo."
Akutero Yehova, amene moto wake uli mu Ziyoni,
ndipo ng'anjo yake ili mu Yerusalemu.

## 32

*Ufumu Wachilungamo*

1 Taonani, kudzakhala mfumu ina imene idzalamulira mwachilungamo,
ndipo akalonga ake adzaweruza molungama.

2 Munthu aliyense adzakhala ngati pothawirapo mphepo
ndi malo obisalirapo namondwe,
adzakhala ngati mitsinje ya m'chipululu,
ngati mthunzi wa thanthwe lalikulu la m'dziko lowuma.

3 Ndipo maso a anthu openya sadzakhalanso otseka,
ndipo makutu a anthu akumva adzamvetsetsa.
4 Anthu a mtima wopupuluma adzadziwa ndi kuchita zinthu mofatsa,
ndipo anthu ovutika kuyankhula adzayankhula mosadodoma ndi momveka.
5 Chitsiru sichidzatchedwanso munthu waulemu wake
ndipo munthu woyipa sadzalemekezedwa.
6 Pakuti munthu opusa amayankhula zauchitsiru,
amaganiza kuchita zoyipa:
Iye amachita zoyipira Mulungu,
ndipo amafalitsa zolakwika zokhudza Yehova;
anjala sawapatsa chakudya
ndipo aludzu sawapatsa madzi.
7 Munthu woyipa njira zake ndi zoyipanso,
iye kwake n'kulingalira zinthu zoyipa.
Amalingalira zakuti awononge anthu aumphawi ndi mabodza ake
ngakhale kuti waumphawiyo akuyankhula zoona.
8 Koma munthu wolemekezeka amalingaliranso kuchita zinthu zabwino,
Iye amakhazikika pa zinthu zabwinozo.

*Akazi a ku Yerusalemu*

9 Khalani maso, inu akazi
amene mukungokhala wopanda kulingalira kuti kunja kulinji
ndipo imvani mawu anga.
Inu akazi odzitama, imvani zimene ndikunena!
10 Pakapita chaka ndi masiku pang'ono
inu akazi amatama mudzanjenjemera;
chifukwa mitengo ya mphesa idzakanika
ndipo zipatso sizidzaoneka.
11 Nthunthumirani inu okhala mosatekesekanu;
ndipo njenjemerani, inu akazi omadzikhulupirira nokhanu.
Vulani zovala zanu,
ndipo valani ziguduli m'chiwuno mwanu.
12 Dzigugudeni pachifuwa mwachisoni chifukwa minda yachonde,
ndi mphesa yawonongeka.
13 M'dziko la anthu anga
mwamera minga ndi mkandankhuku.
Zoona, mulilire nyumba zonse zachikondwerero
ndi mzinda uno umene unali wachisangalalo.
14 Nyumba yaufumu idzasiyidwa,
mzinda waphokoso udzakhala wopanda anthu;
malinga ndi nsanja zidzasanduka chipululu mpaka muyaya.
Abulu adzasangalalamo ndipo ziweto zidzapezamo msipu.
15 Yehova adzatipatsa mzimu wake,
ndipo dziko lachipululu lidzasanduka munda wachonde,
ndipo munda wachonde udzakhala ngati nkhalango.
16 Tsono m'chipululu mudzakhala chiweruzo cholungama
ndipo m'minda yachonde mudzakhala chilungamo.

17 Mtendere udzakhala chipatso chachilungamo;
zotsatira za chilungamo zidzakhala bata ndi kudzidalira mpaka muyaya.
18 Anthu anga adzakhala m'midzi yamtendere,
m'nyumba zodalirika,
ndi malo osatekeseka a mpumulo.
19 Ngakhale nkhalango idzawonongedwa ndi matalala
ndipo mzinda udzagwetsedwa mpaka pansi,
20 inutu mudzakhala odalitsika ndithu.
Mudzadzala mbewu zanu m'mbali mwa mtsinje uliwonse,
ndipo ng'ombe zanu ndi abulu anu zidzadya paliponse.

# 33

*Msautso ndi Thandizo*

1 Tsoka kwa iwe, iwe wowonongawe,
amene sunawonongedwepo!
Tsoka kwa iwe, iwe mthirakuwiri,
iwe amene sunanyengedwepo!
Iwe ukadzaleka kuwononga,
udzawonongedwa,
ukadzasiya um'thirakuwiri, adzakuwononga,
ndipo ukadzaleka kuchita zachinyengo adzakunyenga.

2 Inu Yehova, mutikomere mtima ife;
tikulakalaka Inu.
Tsiku ndi tsiku mutitchinjirize ndi mkono wanu,
ndipo mutipulumutse pa nthawi ya masautso.
3 Mukatulutsa liwu lanu longa bingu mitundu ya anthu imathawa;
pamene Inu mwadzambatuka mitundu ya anthu imabalalika.
4 Zofunkha za ku nkhondo za mitundu ina Aisraeli adzazisonkhanitsa ngati mmene limachitira dzombe.
Iwo adzalumphira zofunkhazo monga mmene limachitira dzombe.

5 Yehova wakwezeka kwambiri pakuti amakhala pamwamba pa zonse
adzadzaza Ziyoni ndi chilungamo ndi chipulumutso.
6 Iye adzakupatsani mtendere pa nthawi yanu,
adzakupatsani chipulumutso chochuluka, nzeru zambiri ndi chidziwitso chochuluka;
kuopa Yehova ngati madalitso.

7 Taonani, anthu awo amphamvu akulira mofuwula m'misewu;
akazembe okhazikitsa mtendere akulira kwambiri.
8 M'misewu yayikulu mulibe anthu,
m'misewu mulibe anthu a paulendo.
Mdaniyo ndi wosasunga pangano.
Iye amanyoza mboni.
Palibe kulemekezana.
9 Dziko likulira ndipo likunka likutha.
Nkhalango ya Lebanoni ikuchita manyazi, yafota.
Chigwa cha chonde cha Saroni chasanduka chachidalala.
Masamba a mitengo ya ku Basani ndi Karimeli akuyoyoka.

10 Yehova akunena kuti, “Tsopano ndidzadzambatuka
ndipo ndidzaonetsa mphamvu zanga,
ndipo ndidzakwezedwa.
11 Zolingalira zanu n’zachabechabe
ngati udzu wamanyowa.
Mpweya wamoto udzakupserezani.
12 Anthu a mitundu ina adzatenthedwa ngati miyala ya njereza;
ndi ngati minga yodulidwa.”

13 Inu amene muli kutali, imvani zimene ndachita;
inu amene muli pafupi, dziwani mphamvu zanga
14 Mu mzinda wa Ziyoni anthu ochimwa agwidwa ndi mantha;
anthu osapembedza Mulungu akunjenjemera:
Iwo akunena kuti, “Ndani wa ife angathe kukhala m’moto wonyeketsa?
Ndani wa ife angathe kukhala moto wosatha?”
15 Angathe kuti ndi amene amachita zolungama
ndi kuyankhula zoona,
amene amakana phindu lolipeza monyenga
ndipo salola manja ake kulandira ziphuphu,
amene amatseka makutu ake kuti angamve mawu opangana kupha anzawo
ndipo amatsinzina kuti angaone zoyipa.
16 Munthu wotere ndiye adzakhale pa nsanja,
kothawira kwake kudzakhala m’malinga a m’mapiri.
Azidzalandira chakudya chake
ndipo madzi sadzamusowa.

17 Nthawi imeneyo maso a ana adzaona mfumu ya maonekedwe wokongola
ndi kuona dziko lotambasukira kutali.
18 Mu mtima mwanu muzidzalingalira zoopsa zinachitika kale zija:
“Ali kuti mkulu wa Asilikali uja?
Ali kuti wokhometsa misonkho uja?
Ali kuti mkulu woyang’anira nsanja?”
19 Simudzawaonanso anthu odzikuza aja,
anthu aja achiyankhulo chosadziwika,
chachilendo ndi chosamveka.

20 Taonani Ziyoni, mzinda wa zikondwerero zachipembedzo chathu;
maso anu adzaona Yerusalemu,
mzinda wamtendere, tenti imene sidzachotsedwa,
zikhomo zake sizidzazulidwa,
kapena zingwe zake kuduka.
21 Kumeneko Yehova adzaonetsa ulemerero wake
ndipo mzindawo udzakhala kasupe wa mitsinje yayikulu.
Ngalawa za zopalasa sizidzapitamo,
sitima zapamadzi zikuluzikulu sizidzayendamo.
22 Pakuti Yehova ndi woweruza wathu,
Yehova ndiye wotilamulira,
Yehova ndiye mfumu yathu;
ndipo ndiye amene adzatipulumutse.

23 Zingwe za sitima zapamadzi za adani athu zamasuka,

sizikutha kulimbitsa mlongoti wake,
matanga ake sakutheka kutambasuka.
Ngakhale tidzagawana zofunkha zochuluka kwambiri
ndipo ngakhale olumala adzatenga zofunkhazo.
24 Palibe ndi mmodzi yemwe wokhala m'Ziyoni adzanene kuti, "Ndikudwala"
ndipo anthu onse okhala m'menemo machimo awo adzakhululukidwa.

# 34

*Chiweruzo cha Anthu a Mitundu Yonse*

1 Inu anthu a mitundu yonse, bwerani pafupi kuti mumve:
tcherani khutu, inu anthu a mitundu ina yonse:
Limvetsere dziko lapansi pamodzi ndi zonse zili m'menemo,
dziko lonse pamodzi ndi zonse zochokera m'menemo!
2 Yehova wayipidwa ndi anthu a mitundu yonse;
wapsera mtima magulu awo onse ankhondo.
Iye adzawawononga kotheratu,
nawapereka kuti aphedwe.
3 Anthu awo ophedwa adzatayidwa kunja,
mitembo yawo idzawola ndi kununkha;
mapiri adzafiira ndi magazi awo.
4 Dzuwa, mwezi ndi nyenyezi zidzasungunuka
ndipo mlengalenga mudzakulungidwa ngati chipepala;
nyenyezi zonse zidzayoyoka
ngati masamba ofota a mphesa,
ngati masamba onyala a mtengo wa mkuyu.

5 Yehova akuti, "Lupanga langa lakhutiratu magazi kumwamba;
taonani, likutsika kudzalanga anthu a ku Edomu,
anthu amene ndawawononga kotheratu."
6 Lupanga la Yehova lakhuta magazi,
lakutidwa ndi mafuta;
magazi a ana ankhosa onenepa ndi ambuzi,
mafuta a ku impsyo za nkhosa zazimuna.
Pakuti Yehova ali ndi nsembe mu Bozira
ndiko kuphedwa kwa anthu ambiri m'dziko la Edomu.
7 Pamodzi ndi anthuwo zidzaphedwanso njati,
ng'ombe zazimuna zazing'ono ndi zazikulu zomwe.
Dziko lawo lidzakhala magazi okhaokha,
ndipo nthaka idzakutidwa ndi mafuta.

8 Iyi ndi nthawi imene Yehova adzalipsira
ndi kulanga adani a Ziyoni.
9 Madzi a m'mitsinje ya Edomu adzasanduka phula,
ndipo fumbi lake lidzasanduka sulufule;
dziko lake lidzasanduka phula lamoto!
10 Motowo sudzazimitsidwa usiku ndi usana;
utsi wake udzafuka kosalekeza.
Dzikolo lidzakhala chipululu pa mibado ndi mibado;
palibe ndi mmodzi yemwe amene adzadutsemo.
11 M'dzikomo mudzakhala akabawi ndi anungu;

amantchichi ndi akhwangwala adzapanga zisa zawo m'menemo.
Mulungu adzatambalitsa pa Edomu
chingwe choyezera cha chisokonezo
ndi chingwe chowongolera cha chiwonongeko.
12 Anthu olemekezeka ake sadzatchedwanso mfumu kumeneko;
akalonga ake onse adzachotsedwa.
13 Minga idzamera m'nyumba zake zankhondo zotetezedwa,
khwisa ndi mitungwi zidzamera m'malinga ake.
Ankhandwe azidzadya m'menemo;
malo okhalamo akadzidzi.
14 Avumbwe adzakumana ndi afisi,
ndipo zirombo za m'chipululu zizidzayitanizana.
Kumeneko kudzafikanso mizimu yoyipa
ndi kupeza malo opumulirako.
15 Kadzidzi adzamangako chisa chake n'kuyikirako mazira,
adzaswa ana ake ndi kusamalira ana ake mu mthunzi wa mapiko ake;
akamtema adzasonkhananso kumeneko,
awiriawiri.
16 Funafunani m'buku la Yehova ndi kuwerenga:
mwa zolengedwazi palibe chimene chidzasowa;
sipadzakhala n'chimodzi chomwe chopanda chinzake.
Pakuti Yehova walamula kuti zitero,
ndipo Mzimu wake udzawasonkhanitsa pamodzi.
17 Yehova wagawa dziko lawo;
wapatsa chilichonse chigawo chake.
Dziko lidzakhala lawo mpaka muyaya
ndipo zidzakhala m'menemo pa mibado yonse.

# 35

*Chimwemwe cha Opulumutsidwa*

1 Chipululu ndi dziko lopanda madzi zidzasangalala;
dziko lowuma lidzakondwa
ndi kuchita maluwa. 2 Dzikolo lidzakhala ndi maluwa ochuluka
lidzasangalala kwambiri ndi kufuwula mwachimwemwe.
Lidzakhala ndi ulemerero monga wa ku mapiri a ku Lebanoni,
maonekedwe ake wokongola adzakhala ngati a ku Karimeli ndi a ku Saroni.

Aliyense adzaona ulemerero wa Yehova,
ukulu wa Mulungu wathu.
3 Limbitsani manja ofowoka,
limbitsani mawondo agwedegwede;
4 nenani kwa a mitima yamantha kuti;
"Limbani mtima, musachite mantha;
Mulungu wanu akubwera,
akubwera kudzalipsira;
ndi kudzabwezera chilango adani anu;
akubwera kudzakupulumutsani."

5 Pamenepo maso a anthu osaona adzapenyanso
ndipo makutu a anthu osamva adzatsekuka.
6 Anthu olumala adzalumpha ngati mbawala,

ndipo osayankhula adzayimba mokondwera.
Akasupe adzatumphuka m'chipululu
ndipo mitsinje idzayenda m'dziko lowuma,
7 mchenga wotentha udzasanduka dziwe,
nthaka yowuma idzasanduka ya akasupe.
Pamene panali mbuto ya ankhandwe
padzamera udzu ndi bango.

8 Ndipo kumeneko kudzakhala msewu waukulu;
ndipo udzatchedwa Msewu Wopatulika.
Anthu odetsedwa
sadzayendamo m'menemo;
zitsiru sizidzasochera m'menemo.
9 Kumeneko sikudzakhala mkango,
ngakhale nyama yolusa sidzafikako;
sidzapezeka konse kumeneko.
Koma okhawo amene Yehova anawapulumutsa adzayenda mu msewu umenewu.
10 Iwo amene Yehova anawawombola adzabwerera.
Adzalowa mu mzinda wa Ziyoni akuyimba;
kumeneko adzakondwa mpaka muyaya.
Adzakutidwa ndi chisangalalo ndi chimwemwe,
ndipo chisoni ndi kudandaula zidzatheratu.

# 36

### *Senakeribu Awopseza Yerusalemu*

1 Chaka cha khumi ndi chinayi cha ulamuliro wa Mfumu Hezekiya,
Senakeribu mfumu ya ku Asiriya anathira nkhondo mizinda yonse
yotetezedwa ya ku Yuda, nayilanda.
2 Kenaka mfumu ya ku Asiriya
inatuma kazembe wake wankhondo pamodzi ndi gulu lalikulu lankhondo kuchokera ku Lakisi kupita kwa mfumu Hezekiya ku Yerusalemu. Tsono kazembeyo anayima pafupi ndi ngalande yamadzi yochokera ku Dziwe lakumtunda pa msewu wopita ku malo a munda wa mmisiri wochapa zovala.
3 Panali anthu atatu. Woyamba anali Eliyakimu mwana wa Hilikiya komanso ndiye woyang'anira nyumba ya mfumu. Wachiwiri anali Sebina amene anali mlembi wa bwalo; ndipo wachitatu anali Yowa mwana wa Asafu komanso anali wolemba zochitika. Anthu awa anatuluka kukakumana ndi kazembe wa ankhondo uja.

4 Kazembe wa ankhondo anawawuza kuti, "Kamuwuzeni Hezekiya kuti,
"Mfumu yayikulu, mfumu ya ku Asiriya ikunena kuti, Kodi
chikukulimbitsa mtima ndi chiyani?
5 Iwe ukuti uli ndi luso ndiponso mphamvu pa nkhondo, komatu ukuyankhula mawu opanda pake. Kodi
tsono iwe ukudalira yani kuti undiwukire ine?
6 Taona tsono, iwe ukudalira Igupto, bango lothyokalo, limene limalasa m'manja mwa munthu ngati waliyesa ndodo yoyendera! Umo ndi mmene Farao
mfumu ya ku Igupto imachitira aliyense amene akuyidalira.
7 Ndipo ngati ukunena kwa ine kuti, 'Ife tikudalira Yehova Mulungu wathu,' kodi si Mulungu yemweyo amene nyumba zake ndi maguwa ake, Hezekiya anachotsa, nawuza anthu a ku Yuda ndi a ku Yerusalemu kuti, 'Muzipembedza pa guwa lansembe ili?'

8 "Ndipo tsopano bwera udzakambirane ndi mbuye wanga, mfumu ya ku Asiriya: Ine ndidzakupatsa akavalo 2,000 ngati ungathe kupeza

okwerapo! 9 Iwe ungathe bwanji kugonjetsa ngakhale mmodzi mwa
akazembe ang'onoang'ono a mbuye wanga, pamene ukudalira Igupto
kuti akupatse magaleta ndi anthu okwera pa akavalo. 10 Kuwonjezera
pamenepa, kodi ine ndabwera kudzathira nkhondo ndi kuwononga
dziko lino popanda chilolezo cha Yehova? Yehova mwini ndiye
anandiwuza kuti ndidzathire nkhondo ndi kuwononga dziko lino."

11 Pamenepo Eliyakimu, Sebina ndi Yowa anawuza kazembeyo kuti,
"Chonde yankhulani kwa atumiki anufe m'Chiaramu, popeza timachimvа.
Musayankhule nafe mu Chihebri kuopa kuti anthu onse amene ali pa
khomapa angamve."

12 Koma kazembeyo anayankha kuti, "Kodi mbuye wanga wandituma
kuti ndidzanene zinthu izi kwa mbuye wanu yekha ndi inu nokha basi?
Ayi, komanso kwa anthu amene akhala pa khomawa. Iwowa adzadya
chimbudzi chawo chomwe ndi kumwa mkodzo wawo womwe monga
momwe mudzachitire inuyonso."

13 Tsono kazembeyo anayimirira nafuwula mu Chihebri kuti, "Imvani
mawu a mfumu yayikulu, mfumu ya ku Asiriya! 14 Zimene mfumu
ikunena ndi izi: Musalole kuti Hezekiya akunamizeni. Iye sangakupulu-
mutseni! 15 Hezekiya asakukakamizeni kudalira Yehova ndi mawu akuti,
'Ndithu, Yehova adzatipulumutsa; ndipo sadzapereka mzindawu m'dzanja
la mfumu ya ku Asiriya.'

16 "Musamumvere Hezekiya. Zimene mfumu ya ku Asiriya ikunena ndi
izi: Pangani mtendere ndi ine ndipo mutuluke mu mzinda. Mukatero
aliyense wa inu adzadya mphesa ndi nkhuyu za m'munda mwake
ndiponso adzamwa madzi a m'chitsime chake, 17 mpaka mfumuyo
itabwera kudzakutengani kupita ku dziko lofanana ndi lanulo, dziko
limene lili ndi tirigu ndi vinyo watsopano, dziko loyenda mkaka ndi uchi.

18 "Inu musalole kuti Hezekiya akusocheretseni pamene iye akuti,
'Yehova adzatipulumutsa.' Kodi alipo mulungu wa anthu a mtundu wina
amene anapulumutsa dziko lake m'dzanja la mfumu ya ku Asiriya? 19 Kodi
ili kuti milungu ya Hamati ndi Aripadi? Ili kuti milungu ya Sefaravaimu?
Kodi inapulumutsa Samariya m'dzanja langa? 20 Kodi ndi milungu iti mwa
milungu yonse ya mayiko awa amene anapulumutsa dziko lake m'dzanja?
Nanga tsono Yehova adzapulumutsa Yerusalemu m'dzanja langa motani?"

21 Koma anthu anakhala chete ndipo sanayankhepo kanthu, chifukwa
mfumu inawalamula kuti, "Musayankhe."

22 Pamenepo anthu atatu aja Eliyakimu, mwana wa Hilikiya amene
ankayang'anira nyumba ya mfumu; Sebina mlembi wa bwalo; ndi Yowa,
mwana wa Asafu mlembi wa zochitika anapita kwa Hezekiya atang'amba
zovala zawo ndipo anamuwuza zonse zimene anayankhula kazembe uja.

# 37

### *Hezekiya Apempha Thandizo kwa Yehova*

1 Mfumu Hezekiya atamva zimenezi, anang'amba zovala zake navala
chiguduli ndipo analowa m'Nyumba ya Yehova. 2 Iye anatuma Eliyakimu
woyang'anira nyumba ya mfumu, Sebina mlembi wa bwalo, ndi ansembe
akuluakulu, onse atavala ziguduli, kwa mneneri Yesaya mwana wa Amozi.
3 Iwo anamuwuza kuti, "Hezekiya akunena kuti, 'Lero ndi tsiku lamavuto,
lachilango ndi lamanyazi. Ife lero tili ngati mayi woyembekezera amene
pofika nthawi yoti achire akupezeka kuti alibe mphamvu zoberekera.'

[4] Mwina Yehova Mulungu wanu adzamva mawu onse a kazembe amene
mbuye wake, mfumu ya ku Asiriya anamutuma kudzanyoza Mulungu
wamoyo, ndipo Mulunguyo adzamulanga chifukwa cha mawu amene
Yehova Mulungu wanu wamva. Choncho pemphererani anthu otsala
amene akanali ndi moyo."
[5] Akuluakulu a mfumu Hezekiya atafika kwa Yesaya, [6] Yesaya
anawawuza kuti, "Kawuzeni mbuye wanu kuti 'Yehova akunena kuti:
Usachite mantha ndi zimene wamva, mawu amene nthumwi za mfumu
ya ku Asiriya zandinyoza nawo Ine. [7] Tamverani! Ine ndidzayika mwa
mfumuyo mzimu wina kotero kuti akadzamva mphekesera ya nkhondo,
adzabwerera ku dziko lake, ndipo Ine ndidzachititsa kuti aphedwe ndi
lupanga kwawo komweko.' "
[8] Kazembe wa ankhondo uja atamva kuti mfumu ya ku Asiriya yachoka
ku Lakisi, iye anabwerera m'mbuyo ndipo anakapeza mfumu ikuchita
nkhondo ndi mzinda wa Libina.
[9] Nthawi imeneyi Senakeribu analandira uthenga wakuti Tirihaka,
mfumu ya ku Kusi akubwera kudzachita naye nkhondo. Atamva zimenezi,
anatumiza amithenga kwa Hezekiya ndi mawu awa: [10] "Kawuzeni
Hezekiya mfumu ya ku Yuda kuti: Usalole kuti Mulungu amene uku-
mudalira akupusitse ponena kuti, 'Yerusalemu sadzaperekedwa m'manja
mwa mfumu ya ku Asiriya.' [11] Ndithudi iwe unamva zimene mafumu a
ku Asiriya akhala akuchitira mayiko onse. Iwo anawawononga kotheratu.
Tsono iwe ndiye ndi kupulumuka? [12] Makolo anga anawononga mizinda
ya Gozani, Harani, Rezefi ndi anthu a ku Edeni amene ankakhala ku
Telasara. Kodi milungu inayi ija anawapulumutsa anthu a mizindayi?
[13] Kodi mafumu a ku Hamati, Aripadi, Safaravaimu, Hena ndi Iva ali kuti?"

### *Pemphero la Hezekiya*

[14] Hezekiya analandira kalata kwa amithenga nayiwerenga pomwepo.
Hezekiya anapita ku Nyumba ya Yehova ndipo anayika kalatayo pamaso
pa Yehova. [15] Ndipo Hezekiya anapemphera kwa Yehova: [16] "Inu Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli, amene mumakhala pa mpando
wanu waufumu pakati pa akerubi, Inu nokha ndiye Mulungu wolamulira
maufumu onse a dziko lapansi. Munalenga kumwamba ndi dziko lapansi.
[17] Inu Yehova tcherani khutu ndipo mumve. Inu Yehova, tsekulani maso
anu ndipo muone. Imvani mawu onse amene Senakeribu watumiza,
kunyoza Mulungu wamoyo.
[18] "Yehova, n'zoonadi kuti mafumu a Asiriya anawononga mitundu
yonse ya anthu ndi mayiko awo. [19] Iwo anaponyera pa moto milungu
yawo ndi kuyiwononga pakuti sinali milungu koma mafano a mitengo ndi
miyala, yopangidwa ndi manja a anthu. [20] Tsono Inu Yehova Mulungu
wathu, tipulumutseni m'dzanja lake kuti maufumu onse a dziko lapansi
adziwe kuti Inu nokha, Inu Yehova, ndiye Mulungu."

### *Yehova Ayankha Pemphero la Hezekiya*

[21] Tsono Yesaya mwana wa Amozi anatumiza uthenga wochokera kwa
Yehova kwa Hezekiya poyankha pemphero lake lokhudza Senakeribu
mfumu ya ku Asiriya. [22] Mawu amene Yehova wayankhula motsutsana
naye ndi awa:

"Mwana wamkazi wa Ziyoni
akukunyoza ndi kukuseka.
Mwana wamkazi wa Yerusalemu,

akupukusa mutu wake pamene iwe ukuthawa.
23 Kodi iwe wanyoza ndi kulalatira ndani?
Kodi iwe wafuwulira
ndi kumuyang'ana monyada ndani?
Watsutsana ndi Woyerayo wa Israeli!
24 Kudzera mwa amithenga ako
iwe wanyoza Ambuye.
Ndipo wanena kuti,
'Ndi magaleta anga ochuluka
ndafika pamwamba pa mapiri,
pamwamba penipeni pa mapiri a Lebanoni.
Ndagwetsa mitengo yamkungudza yayitali kwambiri,
ndi mitengo yabwino kwambiri ya payini.
Ndafika pa msonga pake penipeni,
nkhalango yake yowirira kwambiri.
25 Ndakumba zitsime ku mayiko achilendo
ndi kumva madzi akumeneko
ndi mapazi anga
ndawumitsa mitsinje yonse ya ku Igupto.'

26 "Kodi sunamvepo
kuti zimenezi ndinazikonzeratu kalekale?
Ndinazikonzeratu masiku amakedzana;
tsopano ndazichitadi,
kuti iwe kwako n'kusandutsa mizinda yotetezedwa
kukhala milu ya miyala.
27 Anthu amene ankakhala kumeneko analibenso mphamvu,
ankada nkhawa ndi kuchititsidwa manyazi.
Anali ngati mbewu za m'munda,
ngati udzu wanthete,
ali ngati udzu omera pa denga,
umene mphepo imawumitsa usanakule n'komwe.

28 "Koma Ine ndimadziwa zonse za iwe;
ndimadziwa pamene ukuyima ndi pamene ukukhala; ndimadziwa pamene ukutuluka ndi pamene ukulowa,
ndiponso momwe umandikwiyira Ine.
29 Chifukwa umandikwiyira Ine
ndi kuti mwano wako wamveka m'makutu anga,
ndidzakola mphuno yako ndi mbedza
ndikuyika chitsulo m'kamwa mwako,
ndipo ndidzakubweza pokuyendetsa
njira yomwe unadzera pobwera.
30 "Iwe Hezekiya, chizindikiro chako cha zimene zidzachitike ndi ichi:
"Chaka chino mudzadya zimene zamera zokha,
ndipo chaka chachiwiri zimene zaphukira pa zomera zokha,
koma chaka chachitatu mudzafesa ndi kukolola,
mudzawoka mitengo yamphesa ndi kudya zipatso zake.
31 Anthu a nyumba ya Yuda amene adzatsalire
adzazika mizu yawo pansi ndipo adzabereka zipatso poyera.
32 Pakuti ku Yerusalemu kudzachokera anthu otsala,
ndi ku phiri la Ziyoni gulu la anthu opulumuka.
Changu cha Yehova Wamphamvuzonse

chidzachita zimenezi.
33 "Choncho Yehova akunena izi za mfumu ya ku Asiriya:
"Iye sadzalowa mu mzinda umenewu
kapena kuponyamo muvi uliwonse.
Sadzafika pafupi ndi mzindawu ndi ankhondo ake a zishango
kapena kuwuzinga ndi mitumbira yankhondo.
34 Adzabwerera potsata njira yomwe anadzera pobwera;
sadzalowa mu mzinda umenewu,"
akutero Yehova.
35 "Ine ndidzawuteteza ndi kuwupulumutsa mzindawu,
chifukwa cha Ine mwini ndiponso chifukwa cha pangano ndi mtumiki wanga Davide!"

36 Tsopano mngelo wa Yehova anapita ku misasa ya nkhondo ya ku
Asiriya ndikukapha asilikali 185,000. Podzuka mmawa mwake anthu
anangoona mitembo ponseponse! 37 Choncho Senakeribu mfumu ya ku
Asiriya anasasula misasa n'kuchoka kubwerera kukakhala ku Ninive.
38 Tsiku lina, pamene ankapembedza m'nyumba ya mulungu wake,
Nisiroki, ana ake awiri, Adirameleki ndi Sarezeri anamupha ndi lupanga,
ndipo anathawira m'dziko la Ararati. Ndipo mwana wake Esrahadoni
analowa ufumu m'malo mwake.

# 38

*Kudwala kwa Hezekiya*

1 Nthawi imeneyo Mfumu Hezekiya anadwala ndipo anali pafupi kufa.
Mneneri Yesaya mwana wa Amozi anapita kukamuona ndipo anati
"Yehova akuti: Konza bwino nyumba yako, pakuti ukufa; suchira."
2 Hezekiya anatembenuka nayang'ana kukhoma, napemphera kwa
Yehova kuti, 3 "Inu Yehova, kumbukirani momwe ndayendera pamaso
panu mokhulupirika ndi modzipereka ndipo ndakhala ndikuchita zab-
wino pamaso panu." Ndipo Hezekiya analira mosweka mtima.
4 Ndipo Yehova analamula Yesaya kuti: 5 "Pita kwa Hezekiya ndipo
ukamuwuze kuti, 'Yehova, Mulungu wa kholo lake Davide akuti: Ndamva
pemphero lako ndipo misozi yako ndayiona; ndidzakuwonjezera zaka 15
pa moyo wako. 6 Ndipo ndidzakupulumutsa, iwe pamodzi ndi mzindawu
m'dzanja la mfumu ya ku Asiriya, Ine ndidzawuteteza mzindawu.
7 " 'Ichi ndi chizindikiro cha Yehova kwa iwe kutsimikiza kuti Yehova
adzachita zimene walonjeza: 8 Chithunzithunzi chimene dzuwa liku-
chititsa pa makwerero a Ahazi ndidzachibweza m'mbuyo makwerero
khumi.' " Ndipo chithunzithunzi chinabwerera m'mbuyo makwerero
khumi.
9 Ndakatulo ya Hezekiya mfumu ya ku Yuda imene analemba atadwala
ndi kuchira:
10 Ine ndinaganiza kuti
ndidzapita ku dziko la akufa
pamene moyo ukukoma.
11 Ndinaganiza kuti, "Sindidzaonanso Yehova,
m'dziko la anthu amoyo,
sindidzaonanso mtundu wa anthu
kapena kukhala pamodzi ndi amene amakhala pa dziko lapansi lino.
12 Nyumba yanga yasasuka
ndipo yachotsedwa.
Ngati tenti ya m'busa mwapindapinda moyo wanga,

ngati munthu wowomba nsalu;
kuyambira usana mpaka usiku mwakhala mukundisiya.
13 Ndinkalira kupempha chithandizo usiku wonse mpaka mmawa;
koma Inu Yehova munaphwanya mafupa anga ngati mkango,
ndipo mwakhala mukundisiya.
14 Ndinkalira ngati namzeze kapena chumba,
ndinkabuwula ngati nkhunda yodandaula.
Maso anga anatopa n'kuyang'ana mlengalenga.
Inu Ambuye, ine ndili m'mavuto bwerani mudzandithandize!"

15 Koma ine ndinganene chiyani?
Yehova wayankhula nane, ndipo Iye ndiye wachita zimenezi.
Chifukwa cha kuwawa kwa mtima wanga,
ine ndidzayenda modzichepetsa masiku amoyo wanga onse.
16 Ambuye, masiku anga ali m'manja mwanu.
Mzimu wanga upeza moyo mwa Inu.
Munandichiritsa ndi
kundikhalitsa ndi moyo.
17 Ndithudi, ine ndinamva zowawa zotere
kuti ndikhale ndi moyo;
Inu munandisunga
kuti ndisapite ku dzenje la chiwonongeko
chifukwa mwakhululukira
machimo anga onse.
18 Pakuti akumanda sangathe kukutamandani,
akufa sangayimbe nyimbo yokutamandani.
Iwo amene akutsikira ku dzenje
sangakukhulupirireni.
19 Amoyo, amoyo okha ndiwo amakutamandani,
monga mmene ndikuchitira ine lero lino;
abambo amawuza ana awo za
kukhulupirika kwanu.

20 Yehova watipulumutsa.
Tiyeni tiyimbe ndi zoyimbira za zingwe
masiku onse a moyo wathu
m'Nyumba ya Yehova.

21 Yesaya anati, "Anthu atenge m'bulu wankhunyu ndipo apake pa chithupsacho ndipo Hezekiya adzachira."

22 Hezekiya n'kuti atafunsa kuti, "Kodi chizindikiro chako n'chiyani chotsimikiza kuti ndidzapita ku Nyumba ya Yehova?"

# 39

*Nthumwi Zochokera ku Babuloni*

1 Nthawi imeneyo Merodaki-Baladani, mwana wa Baladani mfumu ya
ku Babuloni anatumiza nthumwi kwa Hezekiya nawapatsira makalata
ndi mphatso, pakuti anamva za kudwala kwake ndi kuti anachira.
2 Hezekiya anawalandira mwasangala ndipo anawaonetsa zonse zimene
zinali m'nyumba zake zosungiramo siliva, golide, zokometsera zakudya,
mafuta abwino kwambiri, zida zonse zankhondo ndiponso zonse zimene
zinkapezeka m'nyumba zake zosungiramo chuma. Panalibe kanthu

kalikonse ka m'nyumba yaufumu kapena mu ufumu wake onse kamene
sanawaonetse.
3 Tsono mneneri Yesaya anapita kwa mfumu Hezekiya ndipo anamu-
funsa kuti, "Kodi anthu aja anakuwuzani chiyani, ndipo anachokera kuti?"
Hezekiya anayankha kuti, "Anachokera ku dziko lakutali, ku Babuloni."
4 Mneneri anafunsanso kuti, "Kodi m'nyumba yanu yaufumu anaonamo
chiyani?"

Hezekiya anati, "Anaona chilichonse cha m'nyumba yanga yaufumu. Palibe ndi chimodzi chomwe za m'nyumba yosungiramo chuma changa chimene sindinawaonetse."
5 Pamenepo Yesaya anati kwa Hezekiya, "Imvani mawu a Yehova
Wamphamvuzonse: 6 Yehova akuti, nthawi idzafika ndithu pamene zonse
za m'nyumba mwanu ndi zonse zimene makolo anu anazisonkhanitsa
mpaka lero lino, zidzatengedwa kupita nazo ku Babuloni. Sipadzatsalapo
ndi kanthu kamodzi komwe. 7 Ndipo ena mwa ana anu, obala inu amene
adzatengedwanso, ndipo adzawasandutsa adindo ofulidwa m'nyumba ya
mfumu ya ku Babuloni."
8 Hezekiya anayankha kuti, "Mawu a Yehova amene mwayankhula ndi
abwino." Ponena izi iye ankaganiza kuti, "Padzakhala mtendere ndi
chitetezo masiku a moyo wanga onse."

# 40

*Mawu a Chitonthozo kwa Anthu a Mulungu*

1 Atonthozeni, atonthozeni anthu anga,
akutero Mulungu wanu.
2 Ayankhuleni moleza mtima anthu a ku Yerusalemu
ndipo muwawuzitse
kuti nthawi ya ukapolo wawo yatha,
tchimo lawo lakhululukidwa.
Ndawalanga mokwanira
chifukwa cha machimo awo onse.

3 Mawu a wofuwula m'chipululu akuti,
"Konzani njira ya Yehova
m'chipululu;
wongolani njira zake;
msewu owongoka wa Mulungu wathu m'dziko lopanda kanthu.
4 Chigwa chilichonse achidzaze.
Phiri lililonse ndi chitunda chilichonse azitsitse;
Dziko lokumbikakumbika alisalaze,
malo azitundazitunda awasandutse zidikha.
5 Ndipo ulemerero wa Yehova udzaonekera,
ndipo mitundu yonse ya anthu idzawuona,
pakuti wanena zimenezi ndi Yehova."

6 Wina ananena kuti, "Lengeza."
Ndipo ine ndinati, "Kodi ndifuwule chiyani?

"Pakuti anthu onse ali ngati udzu
ndipo kukongola kwawo kuli ngati maluwa akuthengo.
7 Udzu umanyala ndipo maluwa amafota
chifukwa cha kuwomba kwa mpweya wa Yehova."

Mawu aja anatinso, “Ndithudi anthu sasiyana ndi udzu.
8 Udzu umanyala ndipo maluwa amafota,
koma mawu a Mulungu wathu adzakhalapo mpaka muyaya.”

9 Iwe amene ukulengeza nkhani yabwino ku Ziyoni,
kwera pa phiri lalitali.
Iwe amene ukulengeza nkhani yabwino ku Yerusalemu,
fuwula kwambiri,
kweza mawu, usachite mantha;
uza mizinda ya ku Yuda kuti,
“Mulungu wanu akubwera!”
10 Taonani, Ambuye Yehova akubwera mwamphamvu,
ndipo dzanja lake likulamulira,
taonani akubwera ndi mphotho yake
watsogoza zofunkha zako za ku nkhondo.
11 Iye adzasamalira nkhosa zake ngati m’busa:
Iye adzasonkhanitsa ana ankhosa aakazi m’manja mwake
ndipo Iye akuwanyamula pachifuwa chake
ndi kutsogolera bwinobwino nkhosa zoyamwitsa.

12 Kodi ndani akhoza kuyeza kuchuluka kwa madzi a m’nyanja ndi chikhatho chake,
kapena kuyeza kutalika kwa mlengalenga ndi dzanja lake?
Ndani akhoza kuyeza dothi lonse la dziko lapansi m’dengu,
kapena kuyeza kulemera kwa
mapiri ndi zitunda ndi pasikelo?
13 Ndani anapereka malangizo kwa Mzimu wa Yehova
kapena kumuphunzitsa Iye monga phungu wake?
14 Kodi Yehova anapemphapo nzeru kwa yani kuti akhale wopenya,
kapena kuti aphunzire njira yoyenera ndi nzeru?
Iye anapempha nzeru kwa yani
ndi njira ya kumvetsa zinthu?

15 Ndithudi mitundu ya anthu ili ngati dontho la madzi ochoka mu mtsuko.
Iwo akungoyesedwa ngati fumbi chabe pa sikelo;
m’manja mwa Yehova zilumba n’zopepuka ngati fumbi.
16 Nkhalango ya ku Lebanoni singakwanire nkhuni zosonkhera moto pa guwa lansembe,
ngakhale nyama zake sizingakwanire kupereka nsembe zopsereza.
17 Pamaso pa Yehova mitundu yonse ya anthu ili ngati chinthu chopanda-pake;
Iye amayiwerengera ngati chinthu chopanda phindu
ndi cha chabechabe.

18 Kodi tsono Mulungu mungamuyerekeze ndi yani?
Kodi mungamufanizire ndi chiyani?
19 Likakhala fano, m’misiri ndiye analipanga
ndipo m’misiri wa golide amalikuta ndi golide
naliveka mkanda wasiliva.
20 M’mphawi amene sangathe kupeza ngakhale chopereka nsembe chotere
amasankha mtengo umene sudzawola,
nafunafuna m’misiri waluso woti

amupangire fano limene silingasunthike.

21 Kodi simukudziwa?
Kodi simunamve?
Kodi sanakuwuzeni kuyambira pachiyambi pomwe?
Kodi simunamvetsetse chiyambire cha dziko lapansi?
22 Yehova amene amakhala pa mpando wake waufumu kumwamba ndiye analenga dziko lapansi,
Iye amaona anthu a dziko lapansi ngati ziwala.
Ndipo anafunyulula mlengalenga ngati nsalu yotchinga,
nayikunga ngati tenti yokhalamo.
23 Amatsitsa pansi mafumu amphamvu
nasandutsa olamula a dziko kukhala achabechabe.
24 Inde, iwo ali ngati mbewu zimene zangodzalidwa kumene
kapena kufesedwa chapompano,
ndi kungoyamba kuzika mizu kumene
ndi pamene mphepo imawombapo n'kuziwumitsa
ndipo kamvuluvulu amaziwulutsa ngati mankhusu.

25 Woyera uja akuti, "Kodi mudzandiyerekeza Ine ndi yani?
Kapena kodi alipo wofanana nane?"
26 Tayang'anani mlengalenga ndipo onani.
Kodi ndani analenga zonsezi mukuzionazi?
Yehova ndiye amene amazitsogolera ngati gulu la ankhondo,
nayitana iliyonse ndi dzina lake.
Ndipo popeza Iye ali ndi nyonga zambiri,
palibe ndi imodzi yomwe imene inasowapo.

27 Iwe Yakobo, chifukwa chiyani umanena
ndi kumadandaula iwe Israeli, kuti,
"Yehova sakudziwa mavuto anga,
Mulungu wanga sakusamala zomwe zikundichitikira ine?"
28 Kodi simukudziwa?
Kodi simunamve?
Yehova ndiye Mulungu wamuyaya,
ndiyenso Mlengi wa dziko lonse lapansi.
Iye sadzatopa kapena kufowoka
ndipo palibe amene angadziwe maganizo ake.
29 Iye amalimbitsa ofowoka
ndipo otopa amawawonjezera mphamvu.
30 Ngakhale achinyamata amalefuka ndi kufowoka,
ndipo achinyamata amapunthwa ndi kugwa;
31 koma iwo amene amakhulupirira Yehova
adzalandira mphamvu zatsopano.
Adzawuluka ngati chiwombankhanga;
adzathamanga koma sadzalefuka,
adzayenda koma sadzatopa konse.

# 41

*Mulungu Thandizo la Israeli*

1 "Khalani chete pamaso panga, inu mayiko a m'mbali mwa nyanja!
Alekeni ayandikire ndi kuyankhula;

tiyeni tikhale pamodzi
kuti atiweruze.

2 "Ndani anadzutsa wochokera kummawa
uja amene ananka napambana kulikonse kumene ankapita?
Iye amapereka anthu a mitundu ina m'manja mwake
ndipo ndi lupanga lake anagonjetsa
ndi kusandutsa mafumu kukhala ngati fumbi
nawamwaza ngati mankhusu ndi uta wake.
3 Amawalondola namayenda mosavutika,
m'njira imene mapazi ake sanayendemo kale.
4 Ndani anachita zimenezi ndi kuzitsiriza,
si uja amene anayambitsa mitundu ya anthu?
Ine Yehova, ndine chiyambi
ndipo potsiriza pake ndidzakhalapo."

5 Mayiko am'mbali mwa nyanja aona zimenezi ndipo akuopa;
anthu a ku mathero a dziko lapansi akunjenjemera.
Akuyandikira pafupi, akubwera;
6 aliyense akuthandiza mnzake
ndipo akuwuza m'bale wake kuti, "Limba mtima!"
7 M'misiri wa matabwa amalimbikitsa m'misiri wa golide,
ndipo iye amene amasalaza fano ndi nyundo
amalimbikitsa amene amalisanja pa chipala.
Ponena za kuwotcherera iye amati, "Zili bwino."
Iye amalikhomerera fanolo ndi misomali kuti lisagwe.

8 "Koma Iwe Israeli mtumiki wanga,
Yakobo amene ndakusankha,
Ndiwe chidzukulu cha Abrahamu bwenzi langa.
9 Ndinakutengani kuchokera ku mapeto a dziko lapansi,
ndinakuyitanani kuchokera ku mbali za kutali za dziko lapansi.
Ine ndinati, 'Iwe ndiwe mtumiki wanga;'
Ndinakusankha ndipo sindinakutaye.
10 Tsono usaope, pakuti Ine ndili nawe;
usataye mtima chifukwa Ine ndine Mulungu wako.
Ndidzakupatsa mphamvu ndipo ndidzakuthandiza,
ndidzakutchinjiriza ndi dzanja langa lamanja logonjetsa.

11 "Onse amene akupsera mtima
adzachita manyazi ndithu ndi kunyazitsidwa;
onse amene akukangana nawe
sadzakhalanso kanthu, adzawonongeka.
12 Udzafunafuna adani ako,
koma sadzapezeka.
Iwo amene akuchita nawe nkhondo
sadzakhalanso kanthu.
13 Pakuti Ine Yehova, ndine Mulungu wako,
amene ndikukugwira dzanja lako lamanja
ndipo ndikuti, usaope;
ndidzakuthandiza.
14 Usachite mantha, iwe Yakobo wofowoka ngati nyongolotsi,
iwe wochepa mphamvu Israeli,

chifukwa Ine ndidzakuthandiza,”
akutero Yehova Mpulumutsi wako, Woyerayo wa Israeli.
15 “Taona, ndidzakusandutsa ngati chipangizo chopunthira tirigu
chatsopano, chakunthwa ndi cha mano ambiri.
Udzanyenya mapiri ndi kuwaphwanyaphwanya,
ndipo zitunda adzazisandutsa ngati mankhusu.
16 Udzawapeta ndipo adzawuluka ndi mphepo komanso
adzamwazika ndi kamvuluvulu.
Koma iwe udzakondwera chifukwa Ine ndine Mulungu wako,
ndipo udzanyadira chifukwa cha Ine Woyerayo wa Israeli:

17 “Pamene amphawi ndi osauka akufunafuna madzi,
koma sakuwapeza;
ndipo kummero kwawo kwawuma ndi ludzu.
Ine Yehova ndidzayankha pemphero lawo;
Ine, Mulungu wa Israeli, sindidzawasiya.
18 Ndidzayendetsa mitsinje m’malo owuma,
ndi akasupe adzatumphuka mu zigwa.
Ndidzasandutsa chipululu kukhala dziwe la madzi
ndipo dziko lowuma kukhala akasupe a madzi.
19 M’chipululu ndidzameretsa
mkungudza, kasiya mchisu ndi mtengo wa Olivi.
M’dziko lowuma ndidzaza mitengo
ya payini, ya mkuyu ndi ya mlombwa,
20 kuti anthu aone ndi kudziwa;
inde, alingalire ndi kumvetsa,
kuti Yehova ndiye wachita zimenezi;
kuti Woyera wa Israeli ndiye anakonza zimenezi.

21 “Yehova akuwuza milungu ina kuti, ‘Fotokozani mlandu wanu.’
Mfumu ya Yakobo ikuti, ‘Perekani umboni wanu.’
22 Bwerani ndi milungu yanu kuti idzatiwuze
zomwe zidzachitike m’tsogolo.
Tifotokozereni zinthu zamakedzana
tiziganizire
ndi kudziwa zotsatira zake.
Kapena tiwuzeni zimene zidzachitike m’tsogolo,
23 tiwuzeni kuti kutsogolo kuli zotani,
ndipo ife tidziwa kuti ndinu milungu.
Chitani chinthu chabwino kapena choyipa,
ndipo mutidabwitsa ndi kutichititsa mantha.
24 Koma inu sindinu kanthu
ndipo zochita zanu n’zopandapake;
amene amapembedza inu ali ngati chinthu chokanidwa chifukwa ndi
choyipa.

25 “Ndinawutsa munthu wina kumpoto ndipo anabwera,
munthu wochokera kummawa amene ndinamuyitana.
Amapondaponda olamulira ngati matope,
ngati ndi wowumba mbiya amene akuponda dongo.
26 Ndani anawululiratu zimenezi poyamba pomwe, kuti ife tidziwe,
kapena kutiwuziratu zisanachitike kuti ife tinene kuti, ‘Analondola?’

Palibe amene ananena,
palibe analengeza zimenezi,
palibe anamva mawu anu.
27 Ine ndinali woyamba kumuwuza Ziyoni kuti, 'Taona, si awa akubwera apawa!'
Ndinatumiza mthenga wa nkhani yabwino ku Yerusalemu.
28 Koma ndikayang'ana palibe ndi mmodzi yemwe,
palibe ndi mmodzi yemwe pakati pawo wotha kupereka uphungu,
palibe woti ayankhe pamene ine ndawafunsa.
29 Taonani, milungu yonseyi ndi yachinyengo!
Zochita zawo si kanthu konse;
mafano awo ali ngati mphepo yachabechabe.

# 42

*Mtumiki wa Yehova*

1 "Nayu mtumiki wanga, amene ndimamuchirikiza,
amene ndamusankha, amenenso ndimakondwera naye.
Ndayika Mzimu wanga mwa Iyeyo,
ndipo adzaweruza anthu a mitundu yonse mwachilungamo.
2 Iye sadzafuwula, sadzamveka mawu,
kapena mawu ake kumveka m'misewu.
3 Bango lophwanyika sadzalithyola,
ndipo moto wozilala sadzawuzimitsa.
Motero adzaonetsa kuti chilungamo ndicho choonadi;
4 sadzafowoka kapena kukhumudwa
mpaka atakhazikitsa chilungamo pa dziko lapansi,
ndi mpaka mayiko a m'mbali mwa nyanja atafika poyembekezera malangizo ake."

5 Yehova Mulungu
amene analenga zamlengalenga ndi kuziyalika,
amene analenga dziko lapansi ndi zonse zimene zimabereka,
amenenso amapereka mpweya kwa anthu ake okhala m'dzikomo,
ndi moyo kwa onse oyendamo, akuti,
6 "Ine Yehova, ndakuyitana chifukwa Ine ndine wolungama;
ndikugwira dzanja ndipo
ndidzakuteteza.
Ndakupereka kukhala pangano langa kwa anthu
ndi kuwunika kwa anthu a mitundu ina.
7 Udzatsekula maso a anthu osaona,
udzamasula anthu a m'ndende
ndi kutulutsa m'ndende anthu okhala mu mdima.

8 "Ine ndine Yehova: dzina langa ndi limenelo!
Sindidzapereka ulemerero wanga kwa wina aliyense
kapena matamando anga kwa mafano.
9 Taonani, zinthu zimene ndinalosera kale zachitikadi,
ndipo ndikuwuzani zinthu zatsopano;
zinthuzo zisanaonekere
Ine ndakudziwitsani."

*Nyimbo Yotamanda Yehova*

10 Imbirani Yehova nyimbo yatsopano,

mutamandeni inu okhala m'dziko lonse lapansi,
inu amene mumayenda pa nyanja, nyanja ikokome ndi zonse zili m'menemo.
Inu okhala pa zilumba tamandani Yehova.
11 Chipululu ndi mizinda yake zikweze mawu awo;
midzi ya Akedara ikondwere.
Anthu a ku Sela ayimbe mwachimwemwe;
afuwule kuchokera pamwamba pa mapiri.
12 Atamande Yehova
ndipo alalike matamando ake kwa anthu apazilumba zonse.
13 Yehova adzapita ku nkhondo ngati munthu wamphamvu,
adzawutsa ukali wake ngati munthu wankhondo;
akukuwa ndiponso akufuwula mfuwu wankhondo
ndipo adzagonjetsa adani ake.

14 Yehova akuti, "Ndakhala ndili chete kwa nthawi yayitali,
ndakhala ndili phee osachita kanthu.
Koma tsopano, ngati mayi pa nthawi yochira,
ndi kubuwula ndi kupuma modukizadukiza ndipo ndili wefuwefu.
15 Ndidzawononga mapiri ndi zitunda
ndipo ndidzawumitsa zomera zawo zonse;
ndidzasandutsa mitsinje kukhala zilumba
ndipo ndidzawumitsa maiwe.
16 Ndidzatsogolera anthu osaona m'misewu imene sanayidziwe,
ndidzawatsogolera m'njira zimene sanayendepo;
ndidzasandutsa mdima wa kutsogolo kwawo kuti ukhale kuwala
ndipo ndidzasalaza malo osalala.
Zimenezi ndizo ndidzachite;
sindidzawataya.
17 Koma onse amene amadalira mafano
amene amanena kwa mafanowo kuti, 'ndinu milungu yathu,'
ndidzawachititsa manyazi kotheratu.

*Aisraeli Alephera Kuphunzira*

18 "Imvani, agonthi inu;
yang'anani osaona inu, kuti muone! 19 Ali wosaona ndani, si mtumiki wanga kodi?
Ndipo ndani ali wosamva ngati mthenga amene ndamutuma?
Kodi ndani ali wosaona ngati uja ndinachita naye pangano,
kapena wosaona ndani ngati mtumiki wa Yehova?
20 Iwe waona zinthu zambiri, koma sunazisamale;
makutu ako ndi otsekuka koma sumva kanthu."
21 Chinamukomera Yehova
chifukwa cha chilungamo chake,
kapena lamulo lake kukhala lalikulu ndi lopambana.
22 Koma awa ndi anthu amene afunkhidwa ndi kuwalanda zinthu zawo,
onsewa anawakola m'maenje
kapena akuwabisa m'ndende.
Tsono asanduka chofunkha
popanda wina wowapulumutsa
kapena kunena kuti,
"Abwezeni kwawo."

23 Kodi ndani wa inu amene adzamvetsera zimenezi
kapena kutchera khutu ndi kumva za m'tsogolomo?
24 Ndani anapereka Yakobo kwa ofunkha,
ndi Israeli kwa anthu akuba?
Kodi si Yehova,
amene ife tamuchimwirayu?
Pakuti sanathe kutsatira njira zake;
ndipo sanamvere malangizo ake.
25 Motero anawakwiyira kwambiri,
nawavutitsa ndi nkhondo.
Anayatsa moto ponseponse mowazungulira komabe iwo sanamvetse;
motowo unawapsereza, koma iwo sanatengepo phunziro ayi.

# 43

*Yehova Yekha Mpulumutsi wa Israeli*

1 Koma tsopano, Yehova
amene anakulenga, iwe Yakobo,
amene anakuwumba, iwe Israeli akuti,
"Usaope, pakuti ndakuwombola;
Ndinakuyitanitsa mokutchula dzina lako, ndiwe wanga.
2 Pamene ukuwoloka nyanja,
ndidzakhala nawe;
ndipo pamene ukuwoloka mitsinje,
sidzakukokolola.
Pamene ukudutsa pa moto,
sudzapsa;
lawi la moto silidzakutentha.
3 Chifukwa Ine Yehova, Mulungu wako,
Woyera wa Israeli, ndine Mpulumutsi wako.
Ndinapereka Igupto pofuna kuti ndiwombole iwe,
ndinapereka Kusi ndi Seba m'malo mwa iwe.
4 Popeza kuti ndiwe wamtengowapatali wolemekezeka ndi wapamtima panga,
ndipo chifukwa ndimakukonda,
ndidzapereka anthu m'malo mwa iwe,
ndidzapereka mitundu ya anthu pofuna kuwombola moyo wako.
5 Usachite mantha, pakuti Ine ndili nawe;
ndidzabweretsa ana ako kuchokera kummawa,
ndipo ndidzakusonkhanitsani kuchokera kumadzulo.
6 Ndidzawuza a kumpoto kuti, 'Amasuleni,'
ndidzawuza akummwera kuti, 'Musawagwire.'
Bweretsani ana anga aamuna kuchokera ku mayiko akutali,
ana anga a akazi kuchokera kumalekezero a dziko lapansi;
7 onsewo amadziwika ndi dzina langa;
ndinawalenga chifukwa cha ulemerero wanga,
ndinawawumba, inde ndinawapanga."
8 Tulutsa anthu amene ali nawo maso koma sakupenya,
anthu amene ali nawo makutu koma sakumva.
9 Mitundu yonse ya anthu isonkhane pamodzi,
anthu a mitundu ina akhale pamodzi pabwalo la milandu.
Ndani wa iwo amene ananeneratu zimenezi?
Ndani wa iwo anatifotokozerapo zinthu zakalekale?

Abweretu ndi mboni zawo kuti adzatsimikizire kuti ananena zoona,
kuti anthu ena amve ndi kunena kuti, “Ndi zoona.”
10 Yehova akunena kuti, “Inu Aisraeli ndinu mboni zanga,
ndi mtumiki wanga amene ndinakusankha,
kuti mundidziwe ndi kundikhulupirira, ndipo mudzamvetsa kuti Mulungu ndine ndekha.
Patsogolo panga sipanapangidwepo mulungu wina,
ngakhale pambuyo panga
sipadzakhalaponso wina.”
11 Akutero Yehova, “Ine, Inetu ndine Yehova,
ndipo palibe Mpulumutsi wina koma Ine ndekha.
12 Ndine amene ndinaneneratu, amene ndinakupulumutsa;
ndine, osati mulungu wina wachilendo pakati panu amene ndinalengezeratu.
Inu ndinu mboni zanga, kuti Ine ndine Mulungu,” akutero Yehova.
13 “Ine ndine Mulungu kuyambira nthawi yamakedzana, ndipo ndidzakhalabe Mulungu ku nthawi zonse.
Palibe amene angathe kuthawa m’manja mwanga,
ndipo chimene ndachita palibe angathe kuchisintha.”

*Chifundo cha Mulungu ndi Kusakhulupirika kwa Israeli*

14 Yehova akuti,
Mpulumutsi wanu, Woyerayo wa Israeli akuti,
“Chifukwa cha inu ndidzatuma gulu lankhondo kukalimbana ndi Babuloni
ndi kukupulumutsani.
Ndidzagwetsa zitseko zonse za mzindawo, ndipo kukondwa kwa anthu ake kudzasanduka kulira.
15 Ine ndine Yehova, Woyera wanu uja,
Mlengi wa Israeli. Ine ndine Mfumu yanu.”

16 Yehova
anapanga njira pa nyanja,
anapanga njira pakati pa madzi amphamvu.
17 Iye anasonkhanitsa magaleta, akavalo,
gulu lankhondo ndi asilikali amphamvu,
ndipo onse anagwa pamenepo, osadzukanso
anazimitsidwa kutheratu ngati chingwe cha nyale. Yehova ameneyu akuti,
18 “Iwalani zinthu zakale;
ndipo musaganizirenso zinthu zimene zinachitika kale.
19 Taonani, Ine ndikuchita zinthu zatsopano!
Tsopano zayamba kale kuoneka; kodi simukuziona?
Ine ndikulambula msewu m’chipululu
ndi kupanga mitsinje m’dziko lowuma.
20 Nyama zakuthengo, nkhandwe ndi akadzidzi
zinandilemekeza.
Ndidzayendetsa mitsinje m’dziko lowuma
kuti ndiwapatse madzi anthu anga
osankhidwa.
21 Anthu amene ndinadziwumbira ndekha
kuti aziyimba nyimbo yotamanda Ine.

22 “Komatu simunapemphera kwa Ine, Inu a m’banja la Yakobo,

munatopa nane, Inu Aisraeli.
23 Simunabweretse kwa Ine nkhosa za nsembe zopsereza,
kapena kundilemekeza ndi nsembe zanu.
Ine sindinakulemetseni pomakupemphani zopereka za chakudya
kapena kukutopetsani pomakupemphani nsembe zofukiza.
24 Simunandigulire bango lonunkhira
kapena kundipatsa Ine mafuta okwanira a nsembe zanu.
Koma inu mwandilemetsa Ine ndi machimo anu
ndipo mwanditopetsa Ine ndi zolakwa zanu.

25 “Ine, Inetu, ndi amene ndimafafaniza
zolakwa zanu, chifukwa cha Ine mwini,
ndipo sindidzakumbukiranso machimo anu.
26 Mundikumbutse zakale,
ndipo titsutsane nkhaniyi pamodzi;
fotokozani mlandu wanu kuti muonetse kuti ndinu osalakwa.
27 Kholo lanu loyamba linachimwa;
ndipo Atsogoleri anu achipembedzo anandiwukira.
28 Chifukwa chake Ine ndidzanyazitsa akuluakulu a Nyumba yanu ya mapemphero,
ndipo ndidzapereka Yakobo kuti awonongedwe
ndi Israeli kuti achitidwe chipongwe.”

# 44

### *Israeli Wosankhidwa wa Yehova*

1 Yehova akuti, “Mvera tsopano, iwe Yakobo, mtumiki wanga,
Israeli, amene ndinakusankha.
2 Yehova
amene anakupanga iwe, anakuwumba iwe m’mimba ya amayi ako,
ndi amene adzakuthandiza iwe. Iye akuti,
Usachite mantha, iwe Yakobo, mtumiki wanga,
Yesuruni, amene ndinakusankha.
3 Pakuti ndidzathira madzi pa nthaka yowuma,
ndi kuyendetsa mitsinje m’dziko lowuma;
ndidzatumiza Mzimu wanga pa ana anu,
ndi kutsitsa madalitso anga pa zidzukulu zanu.
4 Iwo adzakula ngati udzu wothirira bwino
ndi ngati bango lomera m’mbali mwa mitsinje ya madzi oyenda.
5 Wina adzanena kuti, ‘Ine ndine wa Yehova;’
wina adzadzitcha yekha wa banja la Yakobo;
winanso adzalemba pa dzanja lake, ‘Wa Yehova’
ndipo adzadzitcha wa banja la Israeli.

### *Yehova, Osati Mafano*

6 “Yehova Mfumu
ndi Mpulumutsi wa Israeli, Yehova Wamphamvuzonse akuti:
Ine ndine woyamba ndi wotsiriza;
palibenso Mulungu wina koma Ine ndekha.
7 Ndani nanga angafanane ndi Ine? Muloleni kuti ayankhule.
Muloleni andifotokozere ndi kundiyalira bwino lomwe
zimene zinachitika kuyambira pamene ndinkakhazikitsa anthu anga akalekale,
ndi ziti zimene zidzachitike;

inde, muloleni alosere zimene zikubwera.
8 Musanjenjemere, musachite mantha.
Kodi sindinakuwuzeni zimenezi ndi kuzilosera kalekale lomwe?
Inu ndinu mboni zanga. Kodi aliponso Mulungu wina kupatula Ine?
Ayi, palibe Thanthwe linanso limene sindikulidziwa."

9 Onse amene amapanga mafano ngachabe,
ndipo milungu imene amayilemekeza ndi yopanda phindu.
Iwo amene amapembedza mafano ndi wosaona;
ndipo sazindikira kanthu. Choncho adzawachititsa manyazi.
10 Ndani amasema mulungu ndi kuwumba fano,
limene silingamupindulire?
11 Iye pamodzi ndi anzake onse adzawachititsa manyazi;
amisiri a mafano ndi anthu chabe.
Aloleni onse asonkhane ndi kuyima pabwalo la milandu;
onse adzaopsedwa ndipo adzachita manyazi.

12 Mmisiri wa zitsulo amatenga chitsulo
ndipo amachiyika pa makala amoto;
ndi dzanja lake lamphamvu
amachisula pochimenya ndi nyundo.
Pambuyo pake m'misiri uja amamva njala natha mphamvu;
iye samwa madzi, ndipo amalefuka.
13 Mmisiri wa matabwa nayenso amayeza mtengo ndi chingwe
ndipo amajambula chithunzi ndi cholembera;
amasema bwinobwino ndi chipangizo chake
ndipo amachiwongola bwino ndi chida chake.
Amachipanga ngati munthu,
munthu wake wokongola
kuti aliyike m'nyumba yake yachipembedzo.
14 Amagwetsa mitengo ya mkungudza,
mwinanso amatenga mtengo wa payini kapena wa thundu
n'kudzisankhira mtengo wabwino pakati pa mitengo ya m'nkhalango,
ndipo amadzala mtengo wa payini ndi kuwuleka kuti ukule ndi mvula.
15 Mitengoyo munthu amachitako nkhuni;
nthambi zina amasonkhera moto wowotha,
amakolezera moto wophikira buledi
ndi mbali ina ya mtengowo amapangira mulungu ndipo amapembedza;
iye amapanga fano ndi kumaligwadira.
16 Chigawo china cha mtengowo amasonkhera moto
wowotcherapo nyama imene
amadya, nakhuta.
Iye amawotha motowo ndipo amanena kuti,
"Aa! Ndikumva kutentha; pano pali moto."
17 Chigawo chotsala amapanga kamulungu, fano lake limenelo;
amaligwadira ndi kulipembedza.
Amapemphera kwa fanolo ndipo amanena kuti,
"Iwe ndiwe mulungu wanga, ndipulumutse."
18 Anthu otere sadziwa kanthu, samvetsa kanthu kalikonse;
maso awo ndi omatirira ndipo sangathe kuona,
ndipo mitu yawo ndi yogontha kotero sangathe kumvetsa.
19 Palibe amene amayima n'kulingalira.

Palibe wanzeru kapena womvetsa zinthu bwino woti n’kunena kuti,
chigawo china cha mtengowo ndinasonkhera moto;
pa makala ake ndinaphikira buledi,
ndinawotchapo nyama ndipo ndinadya.
Chigawo chotsalachi ndipangire chinthu chonyansachi.
Kodi ndidzagwadira mtengo?
20 Munthu wotere ali ngati wodya phulusa, maganizo ake opusa amusocheretsa;
motero kuti sangathe kudzipulumutsa yekha kapena kudzifunsa kuti,
“Kodi chinthu chili m’manja mwangachi si chabodza?”

21 Yehova akuti, “Iwe Yakobo, kumbukira zinthu izi
popeza kuti ndiwe mtumiki wanga, iwe Israeli.
Ine ndinakupanga iwe, ndiwe mtumiki wanga;
iwe Israeli, sindidzakuyiwala.
22 Ndachotsa zolakwa zako ngati mitambo,
ndi machimo ako ngati nkhungu ya mmawa.
Bwerera kwa Ine,
popeza ndakupulumutsa.”

23 Imbani mwachimwemwe, inu zolengedwa zamlengalenga, pakuti Yehova wachita zimenezi;
fuwula, iwe dziko lapansi.
Imbani nyimbo, inu mapiri,
inu nkhalango ndi mitengo yonse,
chifukwa Yehova wawombola Yakobo,
waonetsa ulemerero wake mwa Israeli.

### *Anthu Adzakhalanso mu Yerusalemu*

24 Yehova Mpulumutsi wanu, amene
anakuwumbani m’mimba ya amayi anu akuti:

“Ine ndine Yehova,
amene anapanga zinthu zonse,
ndinatambasula ndekha zinthu zakuthambo,
ndinayala ndekha dziko lapansi.
25 Ndine amene ndinalepheretsa mipingo ya anthu onyenga,
ndipo ndimapusitsa owombeza mawula.
Ndimasokoneza anthu a nzeru,
ndi kuonetsa kuti nzeru zawo n’zopusa.
26 Ndine amene ndimatsimikiza mawu a atumiki ake
ndi kukwaniritsa zimene analosera amithenga ake.

“Ndine amene ndinanena za Yerusalemu kuti mudzakhalanso anthu.
Ndinanenanso za mizinda ya Yuda kuti idzamangidwanso.
Za mabwinja awo ndinanena kuti ndidzawawutsanso.
27 Ndine amene ndinawuza nyanga yayikulu kuti, ‘Uma’
ndipo ndidzawumitsa mitsinje yako.
28 Ndine amene ndinanena kwa Koresi kuti, ‘Iye ndiye m’busa wanga,’
ndipo adzachita zonse zimene ndikufuna;
iye adzalamula kuti, ‘Yerusalemu amangidwenso’
ndi kuti, ‘Maziko a Nyumba ya Mulungu ayikidwenso.’ ”

# 45

1 Yehova akuyankhula ndi wodzozedwa wake
Koresi amene anamugwira dzanja lamanja
kuti agonjetse mitundu ya anthu
ndi kuwalanda mafumu zida zawo zankhondo,
ndi kutsekula zitseko
kuti zipatazo zisadzatsekedwenso ndi ichi:
2 Ine ndidzayenda patsogolo pako,
ndi kusalaza mapiri;
ndidzaphwanya zitseko za mkuwa
ndi kuthyola mipiringidzo ya chitsulo.
3 Ndidzakupatsa chuma chobisika mu mdima,
katundu wa pamalo obisika,
kotero kuti udziwe kuti Ine ndine Yehova
Mulungu wa Israeli, amene ndakuyitana pokutchula dzina.
4 Chifukwa cha mtumiki wanga Yakobo,
chifukwa cha wosankhidwa wanga Israeli,
Ine ndakuyitana pokutchula dzina
ndipo ndakupatsa dzina laulemu
ngakhale iwe sukundidziwa Ine.
5 Ine ndine Yehova ndipo palibenso wina;
kupatula Ine palibenso Mulungu wina.
Ndidzakupatsa mphamvu,
ngakhale sukundidziwa Ine,
6 kotero kuti kuchokera kummawa mpaka kumadzulo
anthu adzadziwa kuti palibe wina koma Ine ndekha.
Ine ndine Yehova,
ndipo palibenso wina.
7 Ndimalenga kuwala ndi mdima,
ndimabweretsa madalitso ndi tsoka;
ndine Yehova, amene ndimachita zonsezi.

8 “Iwe thambo gwetsa mvula kuchokera kumwamba;
mitambo ivumbwe mivumbi ya chilungamo.
Dziko lapansi litsekuke,
ndipo chipulumutso chiphuke kuti
chilungamo chimereponso;
Ine Yehova, ndine ndalenga zimenezi.

9 “Tsoka kwa wokangana ndi mlengi wake,
ngakhale kuti ali ngati phale chabe pakati pa mapale anzake.
Kodi dongo lingafunse munthu wowumba kuti,
‘Kodi ukuwumba chiyani?’
Kodi ntchito yako inganene kuti,
‘Ulibe luso?’
10 Tsoka kwa wofunsa abambo ake kuti,
‘Kodi munabereka chiyani?’
Kapena amayi ake kuti,
‘Kodi mufuna kubereka chiyani?’

11 “Yehova
Woyerayo wa Israeli, ndiponso Mlengi wake akunena,
zokhudza zinthu zimene zikubwera ndi izi:

Kodi iwe ukundifunsa za ana anga,
kapena kundilamula pa zokhudza ntchito zanga?
12 Ndine amene ndinapanga dziko lapansi
ndikulenga munthu kuti akhalemo.
Ine ndi manja anga ndinayalika thambo;
ndimalamulira zolengedwa zonse za mlengalenga.
13 Ndine amene ndidzawutsa Koresi kuti chilungamo changa chikwaniritsidwe:
ndipo ndidzawongolera njira zake zonse.
Iye adzamanganso mzinda wanga
ndi kumasula anthu anga amene ali mu ukapolo,
wopanda kupereka ndalama kapena mphotho,
akutero Yehova Wamphamvuzonse.”
14 Yehova akuti,
“Chuma cha ku Igupto ndi chuma cha malonda cha Kusi chidzakhala chanu.
Anthu amphamvu zawo ndi athanzi a ku Seba
adzabwera kwa inu
ndipo adzakhala anthu anu;
iwo adzidzakutsatani pambuyo panu
ali m’maunyolo.
Adzakugwadirani
ndi kukupemphani, ponena kuti,
‘Ndithudi Mulungu ali ndi inu, ndipo palibenso wina;
palibenso mulungu wina.’ ”

15 Zoonadi inu muli ndi Mulungu wobisika
amene ali Mulungu ndi Mpulumutsi wa Israeli.
16 Onse amene amapanga mafano adzawachititsa manyazi ndi kuwanyozetsa.
Adzakhala osokonezeka maganizo.
17 Koma Yehova adzapulumutsa Israeli
ndi chipulumutso chamuyaya;
simudzachitanso manyazi kapena kunyozeka
mpaka kalekale.

18 Yehova
analenga zinthu zakumwamba,
Iye ndiye Mulungu;
amene akulenga dziko lapansi,
ndi kulikhazikitsa,
sanalipange kuti likhale lopanda kanthu,
koma analipanga kuti anthu akhalemo.
Iyeyu akunena kuti:
Ine ndine Yehova,
ndipo palibenso wina.
19 Ine sindinayankhule mwachinsinsi,
pamalo ena a mdima;
Ine sindinaziwuze zidzukulu za Yakobo kuti,
“Ndifunefuneni ku malo kopanda kanthu.”
Ine Yehova, ndimayankhula zoona;
ndikunena zolungama.

20 Yehova akuti, "Sonkhanani pamodzi ndipo mubwere;
yandikirani, inu amene munapulumuka pothawa nkhondo kwa anthu a mitundu ina.
Ndinu opanda nzeru amene mumanyamula mafano a mitengo,
amene mumapemphera kwa milungu imene singathe kupulumutsa.
21 Fotokozani mlandu wanu,
mupatsane nzeru nonse pamodzi.
Kodi ndani ananeneratu zimenezi kalekale?
Ndani anazifotokozeratu zimenezi nthawi yamakedzana?
Kodi si Ineyo Yehova?
Ndipo palibenso Mulungu wina kupatula Ine,
Mulungu wolungama ndi Wopulumutsa,
palibenso wina kupatula Ine.

22 "Tembenukirani kwa Ine kuti mupulumuke,
inu anthu onse a pa dziko lapansi,
pakuti Ine ndine Mulungu ndipo palibenso wina.
23 Ndalumbira ndekha,
pakamwa panga patulutsa mawu owona,
mawu amene sadzasinthika konse akuti,
bondo lililonse lidzagwada pamaso panga;
anthu onse adzalumbira potchula dzina langa.
24 Iwo adzanene kwa Ine kuti,
'Chilungamo ndi mphamvu zimapezeka mwa Yehova yekha.' "
Onse amene anamuwukira Iye
adzabwera kwa Iye ndipo adzachita manyazi.
25 Koma mwa Yehova zidzukulu zonse za Israeli
zidzapambana ndi kupeza ulemerero.

# 46

*Za Kupasuka kwa Babuloni ndi Mafano Ake*

1 Beli wagwada pansi, Nebo wawerama;
nyama zonyamula katundu za nyamula milungu yawo.
Mafano awo asanduka katundu wolemera pa msana pa ng'ombe.
Asandukadi ngati katundu pa msana pa nyama zotopa.
2 Nyamazo zikuwerama ndi kufuna kugwa ndi milunguyo;
sizikutha kupulumutsa katunduyo,
izo zomwe zikupita ku ukapolo.
3 Mverani Ine, Inu nyumba ya Yakobo,
inu nonse otsala a m'nyumba ya Israeli,
Ine ndakhala ndi kukusamalirani kuyambira m'mimba ya amayi anu,
ndakhala ndikukunyamulani chibadwire chanu.
4 Mpaka pamene mudzakalambe ndi kumera imvi
ndidzakusamalirani ndithu.
Ndinakulengani ndipo ndidzakunyamulani,
ndidzakusamalirani ndi kukulanditsani.

5 "Kodi inu mudzandifanizira ndi yani, kapena mufananitsa ndi yani?
Kodi mudzandiyerekeza kapena kundifanizitsa ndi yani?
6 Anthu ena amakhuthula golide m'zikwama zawo
ndipo amayeza siliva pa masikelo;
amalemba ntchito m'misiri wosula kuti awapangire mulungu,

kenaka iwo amagwada pansi ndikupembedza kamulunguko.
7 Amanyamula n'kumayenda nayo milunguyo pa mapewa awo;
amayikhazika pa malo pake ndipo imakhala pomwepo.
Singathe kusuntha pamalo pakepo.
Ngakhale wina apemphere kwa milunguyo singathe kuyankha;
kapena kumupulumutsa ku mavuto ake.

8 "Kumbukirani zimenezi ndipo muchite manyazi,
Muzilingalire mu mtima, inu anthu owukira.
9 Kumbukirani zinthu zakale zinthu zamakedzana;
chifukwa Ine ndine Mulungu
ndipo palibe wina ofanana nane.
10 Ndinaneneratu zakumathero kuchokera pachiyambi pomwe.
Kuyambira nthawi yamakedzana ndinaloseratu zoti zidzachitike.
Ndikanena zimene ndifuna kuchita ndipo zimachitikadi.
Chilichonse chimene ndafuna ndimachichita.
11 Ndikuyitana chiwombankhanga kuchokera kummawa.
Ndikuyitana kuchokera ku dziko lakutali munthu amene adzakwaniritsa cholinga changa.
Zimene ndanena ndidzazikwaniritsadi;
zimene ndafuna ndidzazichitadi.
12 Ndimvereni, inu anthu owuma mtima,
inu amene muli kutali ndi chipulumutso.
13 Ndikubweretsa pafupi tsiku la chipulumutso changa;
sichili kutali.
Tsikulo layandikira
ndipo sindidzachedwa kukupulumutsani
ndi kupereka ulemerero wanga kwa Israeli.

# 47

*Kugwa kwa Babuloni*

1 "Tsika, ndi kukhala pa fumbi,
iwe namwali, Babuloni;
khala pansi wopanda mpando waufumu,
iwe namwali, Kaldeya
pakuti sadzakutchulanso wanthete kapena woyenera
kumugwira mosamala.
2 Tenga mphero ndipo upere ufa;
chotsa nsalu yako yophimba nkhope
kwinya chovala chako mpaka ntchafu
ndipo woloka mitsinje.
3 Maliseche ako adzakhala poyera
ndipo udzachita manyazi.
Ndidzabwezera chilango
ndipo palibe amene adzandiletse."

4 Woyerayo wa Israeli ndiye Mpulumutsi wathu,
dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.

5 "Khala chete, ndipo lowa mu mdima,
iwe namwali, Kaldeya;
chifukwa sadzakutchulanso

mfumukazi ya maufumu.
6 Ndinawakwiyira anthu anga,
osawasamalanso.
Ndinawapereka manja mwako,
ndipo iwe sunawachitire chifundo.
Iwe unachitira nkhanza
ngakhale nkhalamba.
7 Iwe unati, ‘Ine ndidzakhalapo nthawi zonse
ngati mfumukazi.’
Koma sunaganizire zinthu izi
kapena kusinkhasinkha za mmene ziti zidzathere.

8 “Ndipo tsopano, tamvera, iwe wongokonda zokondweretsawe,
amene ukukhala mosatekesekawe,
umaganiza mu mtima mwako kuti,
‘Ine ndi Ine, ndipo kupatula ine palibenso wina.
Sindidzakhala konse mkazi wamasiye,
ndipo ana anga sadzamwalira.’
9 Koma m’kamphindi, ndiponso tsiku limodzi,
zinthu ziwiri izi zidzakuchitikira:
ana ako kukufera komanso kukhala mkazi wamasiye.
Zimenezi zidzakuchitikira kwathunthu
ngakhale ali ndi amatsenga ambiri
ndi mawula amphamvu.
10 Iwe unkadalira kuyipa kwako
ndipo unati, ‘Palibe amene akundiona.’
Kuchenjera ndi nzeru zako zidzakusokoneza,
choncho ukuganiza mu mtima mwako kuti,
‘Ine ndine basi, ndipo kupatula ine palibenso wina.’
11 Ngozi yayikulu idzakugwera
ndipo sudzadziwa momwe ungayipewere ndi matsenga ako.
Mavuto adzakugwera
ndipo sudzatha kuwachotsa;
chipasupasu chimene iwe sukuchidziwa
chidzakugwera mwadzidzidzi.

12 “Pitiriza tsono kukhala ndi matsenga ako,
pamodzi ndi nyanga zako zochulukazo,
wakhala ukuzigwiritsa ntchito kuyambira ubwana wako.
Mwina udzatha kupambana
kapena kuopsezera nazo adani ako.
13 Malangizo onse amene unalandira angokutopetsa basi!
Abwere patsogolopa anthu amene amatanthauzira za kumwamba kuti
adzakupulumutseni.
Abwere amene amayang’ana nyenyezi, ndi kumalosera mwezi ndi mwezi
zimene ziti zidzakuchitikire.
14 Ndithudi, anthuwo ali ngati phesi;
adzapsa ndi moto.
Sangathe kudzipulumutsa okha
ku mphamvu ya malawi a moto.
Awa si makala a moto woti wina n’kuwotha;
kapena moto woti wina n’kuwukhalira pafupi.
15 Umu ndi mmene adzachitire amatsenga,

anthu amene wakhala ukugwira nawo ntchito
ndi kuchita nawo malonda chiyambire cha ubwana wako.
Onse adzamwazika ndi mantha,
sipadzakhala ndi mmodzi yemwe wokupulumutsa.”

# 48

*Israeli ndi Nkhutukumve*

1 “Mverani izi, inu nyumba ya Yakobo,
inu amene amakutchani dzina lanu Israeli,
ndinu a fuko la Yuda,
inu mumalumbira m’dzina la Yehova,
ndi kupemphera kwa Mulungu wa Israeli,
ngakhale osati m’choonadi kapena m’chilungamo.
2 Komabe inu mumadzitcha nzika za mzinda wopatulika
ndipo mumadalira Mulungu wa Israeli,
amene dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse:
3 Zimene zinachitika poyamba ndinalosera kalekale,
zinatuluka m’kamwa mwanga ndipo ndinazilengeza;
tsono mwadzidzidzi ndinachitapo kanthu ndipo zinachitikadi.
4 Pakuti Ine ndinadziwa kuti iwe ndiwe nkhutukumve
wa nkhongo gwaa,
wa mutu wowuma.
5 Ine ndinakuwuziratu zinthu izi kalekale lomwe;
zisanachitike ndinazilengezeratu kwa iwe
kuti unganene kuti,
‘Fano langa ndilo lachita zimenezi,
kapena kuti fano langa losema ndi kamulungu kanga kachitsulo ndiwo analamula kuti zimenezi zichitike.’
6 Inu munamva zinthu zimenezi.
Kodi inu simungazivomereze?

“Kuyambira tsopano mpaka m’tsogolo ndidzakuwuzani zinthu zatsopano
zinthu zobisika zimene simunazidziwe konse.
7 Zinthu zimenezi zikulengedwa tsopano lino, osati kalekale;
munali musanazimve mpaka lero lino.
Choncho inu simunganene kuti,
‘Zimenezi ndiye ayi, ndinazidziwa kale.’
8 Inu simunazimvepo kapena kuzidziwa;
makutu anu sanali otsekuka.
Tsono Ine ndinadziwa bwino kuti ndinu anthu achiwembu ndi kuti
chiyambire ubwana wanu munatchedwa owukira.
9 Ine ndikuchedwetsa mkwiyo wanga chifukwa cha dzina langa.
Ndikukulezerani ukali wanga kuti anthu andilemekeze.
Sindidzakuwononganі kotheratu.
10 Taonani, ndinakuyeretsani ngati siliva;
ndinakuyesani m’ng’anjo yamasautso.
11 Chifukwa cha ulemu wanga, chifukwa cha ulemu wanga Ine ndikuchita zimenezi.
Ndingalole bwanji kuti ndinyozeke?
Ulemerero wanga sindidzawupereka kwa wina.

*Kumasulidwa kwa Israeli*

12 “Tamvera Ine, iwe Yakobo,

Israeli, amene ndinakuyitana:
Mulungu uja Woyamba
ndi Wotsiriza ndine.
13 Inde dzanja langa linamanga maziko a dziko lapansi,
dzanja langa lamanja linafunyulula mlengalenga.
Ndi mawu anga ndinalenga kumwamba
ndi dziko lapansi.

14 "Sonkhanani pamodzi inu nonse ndipo mvetserani:
Ndani mwa mafano anu amene analoseratu za zinthu izi?
Wokondedwa wa Yehova uja adzachita
zomwe Iye anakonzera Babuloni;
dzanja lake lidzalimbana ndi Kaldeya.
15 Ine, Inetu, ndayankhula;
ndi kumuyitana
ndidzamubweretsa ndine
ndipo adzakwaniritsa zolinga zake.
16 "Bwerani pafupi ndipo mvetserani izi:
"Kuyambira pachiyambi sindinayankhule mobisa;
pa nthawi imene zinkachitika zimenezi Ine ndinali pomwepo."

Ndipo tsopano Ambuye Yehova wandipatsa Mzimu wake
ndi kunditumа.

17 Yehova, Mpulumutsi wanu,
Woyerayo wa Israeli akuti,
"Ine ndine Yehova Mulungu wanu,
amene ndimakuphunzitsa kuti upindule,
ndimakutsogolera pa njira yoyenera kuyitsata.
18 Ngati iwe ukanangosamalira zolamulira zanga,
bwenzi mtendere wako ukanakhala ngati mtsinje,
ndi chipulumutso chako ngati mafunde a pa nyanja.
19 Zidzukulu zako zikanachuluka ngati mchenga,
ana ako akanachuluka ngati fumbi;
dzina lawo silikanachotsedwa pamaso panga
ndipo silikanafafanizidwa konse."

20 Tulukani m'dziko la Babuloni!
Thawani dziko la Kaldeya!
Lengezani zimenezi ndi mawu a chisangalalo
ndipo muzilalikire
mpaka kumathero a dziko lapansi;
muzinena kuti, "Yehova wawombola Yakobo mtumiki wake."
21 Iwo sanamve ludzu pamene Yehova ankawatsogolera m'chipululu;
anawapatsa madzi otuluka m'thanthwe;
anang'amba thanthwelo ndipo
munatuluka madzi.

22 "Palibe mtendere kwa anthu ochimwa," akutero Yehova.

# 49

*Mtumiki wa Yehova*

1 Mverani Ine, inu anthu a pa zilumba
tcherani khutu, inu anthu a mayiko akutali:
Yehova anandiyitana ine ndisanabadwe,
ananditchula dzina ndili m’mimba ya amayi anga.
2 Iye anasandutsa pakamwa panga kukhala ngati lupanga lakuthwa,
anandibisa mu mthunzi wa dzanja lake;
Iye anandisandutsa ngati muvi wakuthwa
ndipo anandibisa m’chimake.
3 Iye anati kwa ine, “Ndiwe mtumiki wanga, Israeli.
Anthu adzanditamanda chifukwa cha iwe.”
4 Koma Ine ndinati, “Ine ndinkaganiza kuti ndinagwira ntchito
ndi kuwononga mphamvu zanga pachabe,
koma ayi, zondiyenera zili m’manja a Yehova,
ndipo mphotho yanga ili m’manja mwa Mulungu wanga.”

5 Yehova anandiwumba ine
m’mimba mwa amayi anga kuti ndikhale mtumiki wake
kuti ndibweze fuko la Yakobo kwa Iye
ndi kusonkhanitsa Israeli kwa Iye,
choncho ndimalemekezeka m’maso mwa Yehova,
ndipo ndimapeza mphamvu mwa Mulungu wanga.
6 Yehovayo tsono akuti,
“N’chinthu chochepa kwambiri kwa iwe kuti ukhale mtumiki wanga,
kuti udzutse mafuko a Yakobo
ndi kuwabweretsa kwawo Aisraeli amene anapulumuka.
Choncho iwe udzakhala ngati chowunikira,
udzafikitsa uthenga wa chipulumutso changa ku mathero a dziko lapansi.”

7 Yehova Mpulumutsi ndi Woyerayo wa Israeli akuyankhula,
Woyerayo wa Israeli akunena,
amene mitundu ya anthu inamuda,
amenenso anali kapolo wa mafumu ankhanza uja kuti,
“Mafumu adzaona ntchito ya chipulumutso changa ndipo adzayimirira.
Akalonga nawonso adzagwada pansi.
Zimenezi zidzachitika chifukwa cha Yehova amene ndi wokhulupirika
ndi Woyerayo wa Israeli amene wakusankha iwe.”

### *Kubwezeretsedwa kwa Israeli*

8 Yehova akuti,
“Pa nthawi imene ndinakukomera mtima ndinakuyankha,
ndipo pa tsiku lachipulumutso ndinakuthandiza;
ndinakusunga ndi kukusandutsa
kuti ukhale pangano kwa anthu,
kuti dziko libwerere mwakale
ndi kuti cholowa changa chowonongeka chija ndichigawegawenso.
9 Ndidzawuza a m’ndende kuti atuluke
ndi a mu mdima kuti aonekere poyera.

“Adzapeza chakudya m’mphepete mwa njira
ndi msipu pa m’malo owuma.
10 Iwo sadzamva njala kapena ludzu,
kutentha kwa m’chipululu kapena dzuwa silidzawapsereza;

chifukwa Iye amene amawachitira chifundo adzawatsogolera
ndi kuwaperekeza ku akasupe a madzi.
11 Mapiri anga onse ndidzawasandutsa njira yoyendamo,
ndipo misewu yanga yayikulu ndidzayikweza.
12 Taonani, anthu anga adzachokera kutali,
ena kumpoto, ena kumadzulo,
enanso adzachokera ku chigawo cha Asuwani."

13 Imbani mwachimwemwe, inu zolengedwa zamlengalenga;
kondwera, iwe dziko lapansi;
imbani nyimbo inu mapiri!
Pakuti Yehova watonthoza mtima anthu ake,
ndipo wachitira chifundo anthu ake ovutika.

14 Koma Ziyoni anati, "Yehova wandisiya,
Ambuye wandiyiwala."

15 "Kodi amayi angathe kuyiwala mwana wawo wakubere
ndi kusachitira chifundo mwana amene anabereka iwo eni?
Ngakhale iye angathe kuyiwala,
Ine sindidzakuyiwala iwe!
16 Taona, ndakulemba iwe m'zikhantho zanga;
makoma ako ndimawaona nthawi zonse.
17 Amisiri odzakumanganso akubwerera mofulumira,
ndipo amene anakupasula akuchokapo.
18 Kweza maso ako ndipo uyang'aneyang'ane
ana ako onse akusonkhana ndipo akubwera kwa iwe.
Yehova akuti, 'Ine Yehova wamoyo,
anthu ako adzakhala ngati chinthu chodzikongoletsa
chimene mkwatibwi wavala pa mkono pake.'

19 "Ngakhale unasanduka bwinja ndi kuwonongedwa
ndipo dziko lako ndi kusakazidwa,
chifukwa cha kuchuluka kwa anthu malo okhalamo adzakhala operewera
ndipo amene anakuwononga iwe aja adzakhala kutali.
20 Ana obadwa nthawi yako yachisoni
adzanena kuti,
'Malo ano atichepera,
tipatse malo ena woti tikhalemo.'
21 Tsono iwe udzadzifunsa kuti,
'Kodi ndani anandiberekera ana amenewa?
Ana anga onse anamwalira ndipo sindinathenso kukhala ndi ana ena;
ndinapita ku ukapolo ndipo ndinachotsedwa.
Ndani anawalera ana amenewa?
Ndinatsala ndekha,
nanga awa, achokera kuti?' "
22 Zimene Ambuye Yehova akunena ndi izi,
"Taonani, Ine ndidzakodola Anthu a mitundu ina kuti abwere.
Ndidzawakwezera anthu a mitundu ina mbendera yanga kuti abwere.
Tsono adzabwera ndi ana ako aamuna atawanyamula m'manja mwawo
ndipo adzanyamula ana ako aakazi pa mapewa awo.
23 Mafumu adzakhala abambo wongokulera

ndipo akazi a mafumu adzakhala amayi wongokulera.
Iwo adzagwetsa nkhope
zawo pansi.
Ndiye inu mudzazindikira kuti Ine ndine Yehova;
iwo amene amadalira Ine sadzakhumudwa.”

24 Kodi mungathe kulanda anthu ankhondo zofunkha zawo,
kapena kupulumutsa anthu ogwidwa m’dzanja la munthu wankhanza?
25 Koma zimene Yehova akunena ndi izi,
“Ankhondo adzawalanda am’ndende awo,
ndipo munthu woopsa adzamulanda zofunkha zawo;
ndidzalimbana ndi amene amalimbana nanu,
ndipo ndidzapulumutsa ana anu.
26 Anthu amene anakuponderezani adzadya mnofu wawo omwe;
adzamwa magazi awo omwe ngati aledzera ndi vinyo.
Zikadzatero anthu onse adzadziwa
kuti Ine Yehova, ndine Mpulumutsi wanu,
Momboli wanu, Wamphamvu wa Yakobo.”

# 50

*Tchimo la Israeli, Kumvera kwa Mtumiki*

1 Yehova akuti,
“Kalata imene ndinasudzulira amayi
anu ili kuti?
Kapena mwa anthu amene ndili nawo ngongole,
ndinakugulitsani kwa ati?
Inu munagulitsidwa ku ukapolo chifukwa cha machimo anu;
amayi anu anachotsedwa chifukwa cha kulakwa kwanu.
2 N’chifukwa chiyani pamene ndinabwera kudzakupulumutsani panalibe munthu?
Pamene ndinayitana, n’chifukwa chiyani panalibe wondiyankha?
Kodi dzanja langa ndi lalifupi kuti n’kulephera kukuwombolani?
Kodi ndilibe mphamvu zokupulumutsirani?
Ndi kudzudzula kokha ndinawumitsa nyanja yayikulu,
mitsinje ndinayisandutsa chipululu;
nsomba za m’menemo zinawola chifukwa chosowa madzi;
ndipo zinafa ndi ludzu.
3 Ndinaphimba thambo ndi mdima
ndipo chiguduli chinakhala chofunda chake.”

4 Ambuye Yehova anandiphunzitsa mawu oyenera kuyankhula
kudziwa mawu olimbitsa mtima anthu ofowoka.
Mmawa mulimonse amandidzutsa,
amathwetsa khutu langa kuti ndimve monga amachitira munthu amene akuphunzira.
5 Ambuye Yehova wanditsekula makutu anga,
ndipo sindinakhale munthu wowukira
ndipo sindinabwerere m’mbuyo.
6 Ndinapereka msana wanga kwa ondimenya
masaya anga ndinawapereka kwa anthu ondizula ndevu;
sindinawabisire nkhope yanga

anthu ondinyoza ndi ondilavulira.
7 Popeza Ambuye Yehova amandithandiza,
sindidzachita manyazi.
Tsono ndalimba mtima ngati msangalabwi,
chifukwa ndikudziwa kuti sindidzachita manyazi.
8 Wondikhalira kumbuyo ali pafupi,
ndaninso amene adzandiyimba mlandu?
Abwere kuti tionane maso ndi maso!
Mdani wanga ndi ndani?
Abweretu kuti tilimbane!
9 Ambuye Yehova ndiye amene amandithandiza.
Ndaninso amene adzanditsutsa?
Onse adzatha ngati chovala
chodyedwa ndi njenjete.

10 Ndani mwa inu amaopa Yehova
ndi kumvera mawu a mtumiki wake?
Aliyense woyenda mu mdima,
popanda chomuwunikira,
iye akhulupirire dzina la Yehova
ndi kudalira Mulungu wake.
11 Koma tsopano inu nonse amene mumasonkha moto
ndi kuyatsa sakali za moto kufuna kuwononga anzanu,
lowani m'moto wanu womwewo.
Pitani mu sakali za moto zimene mwayatsa.
Ndipo ine Yehova
ndiye amene ndidzakugwetsereni mazunzowo.

# 51

*Chipulumutso Chamuyaya cha Ziyoni*

1 “Mverani Ine, inu amene mukufuna chipulumutso
ndiponso amene mumafunafuna Yehova:
Taganizani za thanthwe kumene munasemedwa
ndipo ku ngwenya kumene anakukumbani;
2 taganizani za Abrahamu, kholo lanu,
ndi Sara, amene anakubalani.
Pamene ndinkamuyitana n'kuti alibe mwana,
koma ndinamudalitsa ndi kumupatsa ana ambiri.
3 Yehova adzatonthozadi Ziyoni,
ndipo adzachitira chifundo mabwinja ake onse;
Dziko lake la chipululu adzalisandutsa ngati Edeni,
malo ake owuma ngati munda wa Yehova.
Anthu adzayimba nyimbo zonditamanda
ndi kundiyamika.

4 “Mverani Ine, anthu anga:
tcherani khutu, inu mtundu wanga:
malangizo adzachokera kwa Ine;
cholungama changa chidzawunikira anthu a mitundu yonse.
5 Ndili pafupi kubwera kudzawombola anthu anga.
Ndidzabwera mofulumira ngati kuwunika kudzapulumutsa anthu anga;

ndipo ndidzalamulira anthu a mitundu yonse.
Mayiko akutali akundiyembekezera.
Iwo akudikira kuti ndidzawapulumutse.
6 Kwezani maso anu mlengalenga,
yang'anani pansi pa dziko;
mlengalenga udzazimirira ngati utsi,
dziko lapansi lidzatha ngati chovala
ndipo anthu ake adzafa ngati nsabwe.
Koma chipulumutso changa chidzakhala mpaka muyaya,
chilungamo changa chidzakhala cha nthawi zonse.

7 "Mverani Ine, inu amene mukudziwa choonadi,
anthu inu amene mukusunga malangizo anga m'mitima yanu;
musaope kudzudzulidwa ndi anthu
kapena kuopsezedwa akamakulalatirani.
8 Pakuti njenjete idzawadya ngati chovala;
mbozi idzawadya ngati thonje.
Koma chilungamo changa chidzakhala mpaka muyaya,
chipulumutso changa chidzakhala mpaka mibadomibado."

9 Dzambatukani, dzambatukani! Valani zilimbe,
Inu Yehova;
dzambatukani, monga munkachitira masiku amakedzana,
monga nthawi ya mibado yakale.
Si ndinu kodi amene munaduladula Rahabe,
amene munabaya chinjoka cha m'nyanja chija?
10 Kodi sindinu amene munawumitsa nyanja yayikulu,
madzi ozama kwambiri aja?
Kodi sindinu amene munapanga njira pa madzi ozama,
kuti anthu amene munawapulumutsa awoloke powuma?
11 Anthu amene Yehova anawawombola adzabwerera
nakafika ku Ziyoni nyimbo ili pakamwa;
chimwemwe chamuyaya chizidzaonekera pa nkhope zawo.
Adzakhala ndi chikondwerero ndi chimwemwe,
chisoni ndi kubuwula zidzathawa.

12 Yehova akuti, "Ndinetu amene ndimakutonthozani mtima.
Chifukwa chiyani mukuopa munthu woti adzafa?
Mukuopa munthu woti monga udzu sadzakhalitsa.
13 Koma inu mumayiwala Yehova Mlengi wanu,
amene anayala za mlengalenga
ndi kuyika maziko a dziko lapansi.
Inu nthawi zonse mumaopsezedwa
chifukwa cha ukali wa anthu okuponderezani
amene angofuna kukuwonongani.
Kodi uli kuti tsopano ukali wa anthu okuponderezaniwo?
14 Am'ndende adzamasulidwa posachedwa;
sadzalowa m'manda awo,
kapena kusowa chakudya.
15 Pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu,
amene ndimavundula nyanja kotero mafunde ake amakokoma.
Dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.
16 Ndayika mawu anga m'kamwa mwanu

ndipo ndakuphimbani ndi mthunzi wa dzanja langa.
Ine ndimayika pa malo pake zinthu za mlengalenga,
ndipo ndinayika maziko a dziko lapansi,
ndimawuza anthu a ku Ziyoni kuti, 'Ndinu anthu anga.' "

*Kutha kwa Mavuto A Yerusalemu*

17 Dzambatuka, dzambatuka!
Imirira iwe Yerusalemu.
Iwe amene wamwa chikho cha mkwiyo
chimene Yehova anakupatsa.
Iwe amene unagugudiza
chikho chochititsa chizwezwe.
18 Mwa ana onse amene anabereka,
panalibe ndi mmodzi yemwe anamutsogolera;
mwa ana onse amene analera,
panalibe ndi mmodzi yemwe anamugwira dzanja.
19 Mavuto awiriwa akugwera iwe.
Dziko lako lasakazika ndi kuwonongeka. Anthu afa ndi njala ndi lupanga.
Ndani angakumvere chisoni?
Ndani angakutonthoze?
20 Ana ako akomoka;
ali lambalamba pa msewu,
ngati mphoyo yogwidwa mu ukonde.
Ukali wa Yehova
ndi chidzudzulo chake zidzawagwera.

21 N'chifukwa chake imva izi iwe amene ukuvutika,
iwe amene waledzera, koma osati ndi vinyo.
22 Ambuye Yehova wanu,
Mulungu amene amateteza anthu ake akuti,
"Taona, ndachotsa m'dzanja lako
chikho chimene chimakuchititsa kudzandira;
sudzamwanso chikho
cha ukali wanga.
23 Ndidzapereka chikhocho kwa anthu amene amakuzunza,
amene ankakuwuza kuti,
'gona pansi tikuyende pa msana.'
Ndipo msana wako anawuyesa pansi popondapo,
ngati msewu woti ayendepo."

# 52

1 Dzambatuka, dzambatuka iwe Ziyoni,
vala zilimbe.
Vala zovala zako zokongola,
iwe Yerusalemu, mzinda wopatulika.
Pakuti kuyambira tsopano anthu osachita mdulidwe ndi odetsedwa
sadzalowanso pa zipata zako.
2 Sasa fumbi lako;
imirira nukhale pa mpando waufumu, iwe Yerusalemu.
Inu omangidwa a ku Ziyoni,
masulani maunyolo amene ali m'khosi mwanumo.
3 Pakuti Yehova akuti,
"Sindinalandirepo kanthu pamene ndinakugulitsani,

choncho mudzawomboledwa wopanda ndalama.”
4 Pakuti Ambuye Yehova akuti,
“Poyamba paja anthu anga anapita kukakhala ku Igupto;
nawonso Asiriya awapondereza popanda chifukwa.”
5 Tsopano Ine Yehova ndikuti,
“Kodi nditani pakuti anthu anga atengedwa ukapolo osaperekapo kanthu,
amene amawalamulira amawanyoza,”
akutero Yehova.
“Ndipo tsiku lonse, akungokhalira
kuchita chipongwe dzina langa.
6 Tsono tsiku limenelo anthu anga adzadziwa dzina langa;
kotero adzadziwa
kuti ndi Ine amene ndikuyankhula,
Indedi, ndine.”

7 Ngokongoladi mapazi a
amithenga obweretsa nkhani yabwino amene akuyenda pa mapiri.
Iwo akukubweretserani nkhani zabwino za mtendere,
chisangalalo ndi chipulumutso.
Iwo akubwera kudzawuza anthu
a ku Ziyoni kuti,
“Mulungu wako ndi mfumu!”
8 Mverani! Alonda anu akukweza mawu awo;
akuyimba pamodzi mwachimwemwe.
Popeza akuona chamaso
kubwera kwa Yehova ku Yerusalemu.
9 Imbani pamodzi mofuwula nyimbo zachimwemwe,
inu mabwinja a Yerusalemu,
pakuti Yehova watonthoza mtima anthu ake,
wapulumutsa Yerusalemu.
10 Yehova wagwiritsa ntchito mphamvu zake zopatulika
pamaso pa anthu a mitundu yonse,
ndipo anthu onse a dziko lapansi
adzaona chipulumutso cha Mulungu wathu.

11 Nyamukani, nyamukani, chokaniko ku Babuloniko!
Musakhudze kanthu kodetsedwa!
Inu amene mumanyamula ziwiya za Yehova
tulukanimo ndipo mudziyeretse.
12 Koma simudzachoka mofulumira
kapena kuchita chothawa;
pakuti Yehova adzayenda patsogolo panu,
Mulungu wa Israeli adzakutetezani kumbuyo kwanu.

### *Kuzunzika ndi Ulemerero wa Mtumiki*

13 Taonani, mtumiki wanga adzapambana pa ntchito yake
adzakwezedwa ndi kulemekezedwa ndipo adzalandira ulemu waukulu kwambiri.
14 Anthu ambiri atamuona anadzidzimuka,
chifukwa nkhope yake inali itasakazika; sinalinso ngati ya munthu.
Ndipo thupi lake linasakazika; silinalinso ngati la munthu.
15 Momwemonso anthu a mitundu yonse adzadodoma naye,
ndipo mafumu adzatseka pakamwa pawo kusowa chonena chifukwa cha iye.

Pakuti zinthu zimene iwo sanawuzidwepo, adzaziona,
ndipo zimene sanazimvepo, adzazimvetsa.

## 53

1 Ndani wakhulupirira zimene tanenazi;
kapena ndani amene Yehova wamuzindikiritsa mphamvu zake?
2 Iye anakula ngati mphukira pamaso pake,
ndiponso ngati muzu m'nthaka yowuma.
Iye analibe thupi labwino kapena nkhope yokongola yoti ife n'kumamuchewukira,
analibe maonekedwe woti ife n'kumamukhumbira.
3 Iye ananyozedwa ndi kukanidwa ndi anthu,
munthu amene moyo wake unali wamasautso, wozolowera zowawa,
ndipo anali ngati munthu amene anzake amaphimba nkhope zawo akamuona.
Iye ananyozedwa, ndipo ife sitinamuyese kanthu.

4 Ndithudi, iye anamva zowawa m'malo mwa ife;
ndipo anasautsidwa m'malo mwathu.
Koma ife tinkaganiza kuti ndi Mulungu amene akumulanga,
kumukantha ndi kumusautsa.
5 Koma iye analasidwa chifukwa cha zolakwa zathu,
ndipo anamuzunza chifukwa cha zoyipa zathu;
iye analangidwa kuti ife tikhale ndi mtendere,
ndipo ndi mabala ake ife tinachiritsidwa.
6 Ife tonse, ngati nkhosa, tasochera,
aliyense mwa ife akungodziyendera;
ndipo Yehova wamusenzetsa
zoyipa zathu zonse.

7 Anthu anamuzunza ndi kumusautsa,
koma sanayankhule kanthu.
Monga mwana wankhosa wopita naye kokamupha amachitira,
kapena monga nkhosa imakhalira duu poyimeta,
momwemonso iye sanatsekule pakamwa pake.
8 Atatha kumugwira mwankhanza ndikumuyimba mlandu, kenaka anapita naye kukamupha.
Ndipo ndani amene analabadirako za zidzukulu zake,
poona kuti iye anachotsedwa m'dziko la anthu amoyo?
Ndani anaganizirapo poona kuti iye anakanthidwa chifukwa cha zolakwa za anthu anga?
9 Anamukonzera manda ake pamodzi ndi anthu oyipa
ndipo anamuyika m'manda pamodzi ndi anthu achuma,
ngakhale kuti iye sanachite za chiwawa,
kapena kuyankhula za chinyengo.

10 Komatu ndi Yehova amene anafuna kuti amuzunze ndi kumusautsa.
Yehova anapereka moyo wa mtumiki wake kuti ukhale nsembe yoperekedwa chifukwa cha zolakwa.
Tsono iye adzaona zidzukulu zake ndipo adzakhala ndi moyo wautali,
ndipo chifuniro cha Yehova chidzachitika mwa iye.
11 Atatha mazunzo a moyo wake,

adzaona kuwala, ndipo adzakhutira.
Mwa nzeru zake mtumiki wanga wolungamayo adzalungamitsa anthu ambiri,
popeza adzasenza zolakwa zawo.
12 Motero Ine ndidzamupatsa ulemu pamodzi ndi akuluakulu,
adzagawana zofunkha ndi ankhondo amphamvu,
popeza anapereka moyo wake mpaka kufa,
ndipo anamuyika m'gulu la anthu olakwa kuti akhululukidwe.
Pakuti iye anasenza machimo a anthu ambiri,
ndipo anawapempherera anthu olakwa.

# 54

*Ulemerero Wam'tsogolo wa Ziyoni*

1 "Sangalala, iwe mayi wosabala,
iwe amene sunabalepo mwana;
imba nyimbo, ndi kufuwula mwachimwemwe,
iwe amene sunamvepo ululu wa pobereka;
chifukwa mkazi wosiyidwa adzakhala ndi ana ambiri
kuposa mkazi wokwatiwa,"
akutero Yehova.
2 Kulitsa malo omangapo tenti yako,
tambasula kwambiri nsalu zake,
usaleke;
talikitsa zingwe zako,
limbitsa zikhomo zako.
3 Pakuti udzasendeza malire ako kumanja ndi kumanzere;
ndipo zidzukulu zako zidzalanda dziko la anthu a mitundu ina
ndipo zidzakhala m'mizinda yawo yosiyidwa.

4 "Usachite mantha; sadzakunyozanso.
Usakhumudwe; sudzapeputsidwanso.
Udzayiwala za manyazi zimene zinakuchitikira nthawi ya unyamata wako
ndipo za manyazi zimene zinakuchitikira pa nthawi ya umasiye wako sudzazikumbukanso.
5 Pakuti Mlengi wako ali ngati mwamuna wako,
dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.
Woyerayo wa Israeli ndiye Mpulumutsi wanu;
dzina lake ndi Mulungu wa dziko lonse lapansi.
6 Yehova wakuyitananso,
uli ngati mkazi wosiyidwa ndi wodzaza ndi chisoni mu mtima,
mkazi amene anakwatiwa pa unyamata wake kenaka n'kukanidwa,"
akutero Mulungu wako.
7 "Kwa kanthawi kochepa, Ine ndinakusiya,
koma ndidzakutenganso chifukwa ndimakukonda kwambiri.
8 Ndinakufulatira kwa kanthawi kochepa
ndili wokwiya kwambiri.
Koma ndi kukoma mtima kwanga kwa muyaya,
ndidzakuchitira chifundo,"
akutero Yehova Mpulumutsi wako.

9 "Kwa ine zimenezi zili ngati mmene zinalili m'nthawi ya Nowa.

Monga ndinalumbira nthawi imeneyo kuti sindidzawononganso dziko lapansi ndi madzi.
Kotero tsopano ndalumbira kuti sindidzakupseraninso mtima,
sindidzakudzudzulaninso.
10 Ngakhale mapiri atagwedezeka
ndi zitunda kusunthidwa,
koma chikondi changa chosasinthika pa iwe sichidzatha.
Pangano langa lamtendere silidzasintha,"
akutero Yehova amene amakuchitira chifundo.

11 "Iwe mzinda wozunzika, wokunthidwa ndi namondwe ndiponso wopanda wokutonthoza,
Ine ndidzakongoletsa miyala yako.
Maziko ako ndidzamanga ndi miyala ya safiro.
12 Ndidzamanga nsanja zako zankhondo ndi miyala yokongola ya rubi.
Ndidzamanga zipata zako ndi miyala yonyezimira ngati moto,
ndipo linga lako lonse lidzakhala la miyala yamtengowapatali.
13 Yehova adzaphunzitsa ana ako onse,
ndipo ana ako adzakhala ndi mtendere wochuluka.
14 Udzakhazikika m'chilungamo chenicheni:
Sudzakhalanso wopanikizika,
chifukwa sudzaopa kanthu kalikonse.
Sudzakhalanso ndi mantha
chifukwa manthawo sadzafika pafupi ndi iwe.
15 Ngati wina adzakuthirani nkhondo, si ndine amene ndachititsa;
aliyense amene adzalimbana nanu adzagonja chifukwa cha iwe.

16 "Taona, ndi Ine amene ndinalenga munthu wosula zitsulo
amene amakoleza moto wamakala
ndi kusula zida zoti azigwiritse ntchito.
Ndipo ndine amene ndinalenga munthu wosakaza kuti awononge;
17 palibe chida chopangidwa ndi mdani chimene chidzakupweteke,
ndipo onse okuneneza pa mlandu udzawatsutsa.
Umu ndimo adzapezekere atumiki a Yehova.
Chipambano chawo chichokera kwa Ine,"
akutero Yehova.

# 55

*Kuyitanidwa kwa Womva Ludzu*

1 "Bwerani, inu nonse amene muli ndi ludzu,
bwerani madzi alipo;
ndipo inu amene mulibe ndalama
bwerani, mudzagule chakudya kuti mudye!
Bwerani mudzagule vinyo ndi mkaka
osalipira ndalama, osalipira chilichonse.
2 Chifukwa chiyani ndalama zanu mukuwonongera zinthu zimene samadya,
ndipo mukuwononga malipiro anu pa zinthu zimene sizikhutitsa?
Tamverani, mvetsetsani zimene ndikunena kuti mudye zimene zili zabwino;
ndipo mudzisangalatse.
3 Tcherani makutu ndipo mubwere kwa Ine;

mvereni Ine, kuti mukhale ndi moyo.
Ndidzachita nanu pangano losatha,
chikondi changa chija chosasinthika ndi chodalirika ndinalonjeza Davide.
4 Taonani, ine ndamusankha kuti akhale mboni yanga kwa mitundu ya anthu,
kuti akhale mtsogoleri ndi wolamulira mitundu ya anthu.
5 Ndithu inu mudzayitanitsa mitundu ya anthu imene simuyidziwa,
ndipo mitundu ya anthu imene sikudziwani idzabwera ndi liwiro kwa inu.
Izi zidzatero chifukwa Yehova Mulungu wanu,
Woyerayo wa Israeli,
wakuvekani ulemerero."

6 Funafunani Yehova pamene Iye akupezeka.
Mupemphere kwa Iye pamene ali pafupi.
7 Woyipa asiye makhalidwe ake oyipa,
ndipo wosalungama asinthe maganizo ake oyipa.
Abwerere kwa Yehova, ndipo adzamuchitira chifundo,
ndi kwa Mulungu wathu, pakuti adzamukhululukira koposa.

8 "Pakuti maganizo anga siwofanana ndi maganizo anu,
ngakhale njira zanu si njira zanga,"
akutero Yehova.
9 "Monga momwe mlengalenga muli kutali ndi dziko lapansi,
momwemonso zochita zanga n'zolekana kutali ndi zochita zanu,
ndipo maganizo anga ndi osiyana kutali ndi maganizo anu.
10 Monga mvula ndi chisanu chowundana
zimatsika kuchokera kumwamba,
ndipo sizibwerera komweko
koma zimathirira dziko lapansi.
Ndipo zimameretsa ndi kukulitsa zomera
kenaka n'kupatsa mlimi mbewu ndi chakudya.
11 Ndi mmenenso amachitira mawu ochokera m'kamwa mwanga.
Sadzabwerera kwa Ine kopanda phindu lake,
koma adzachita zonse zimene ndifuna,
ndipo adzakwaniritsa cholinga chimene ndinawatumira.
12 Inu mudzatuluka mu mzindawo mwachimwemwe
ndipo adzakutsogolerani mwamtendere;
mapiri ndi zitunda
zidzakuyimbirani nyimbo,
ndipo mitengo yonse yam'thengo
idzakuwombereni m'manja.
13 M'malo m'mene tsopano muli mitengo ya minga mudzamera mitengo ya payini,
ndipo kumene kuli mkandankhuku kudzamera mchisu.
Zimenezi zidzakhala chikumbutso cha Yehova,
ngati chizindikiro chamuyaya,
chimene sichidzafafanizika konse."

# 56

*Chipulumutso kwa Anthu Ena Onse*

1 Yehova akuti,

“Chitani chilungamo
ndi zinthu zabwino,
chifukwa chipulumutso changa chili pafupi
ndipo ndidzakuwombolani posachedwapa.
2 Ndi wodala munthu amene amachita zimenezi,
munthu amene amalimbika kuzichita,
amene amasunga Sabata osaliyipitsa,
ndipo amadziletsa kuchita zoyipa.”

3 Mlendo amene waphatikana ndi Yehova asanene kuti,
“Ndithu Yehova wandichotsa pakati pa anthu ake.”
Ndipo munthu wofulidwa asanene kuti,
“Ine ndine mtengo wowuma basi.”
4 Popeza Yehova akuti,
“Wofulidwa amene amasunga masabata anga,
nachita zokomera Ine
ndi kusunga pangano langa,
5 ndidzawapatsa dzina ndi mbiri yabwino
m’kati mwa Nyumba yanga ndi makoma ake,
kuposa kukhala ndi ana aamuna ndi aakazi.
Ndidzawapatsa dzina labwino,
losatha ndi losayiwalika.”
6 Yehova akuti, “Alendo amene amadziphatika kwa Yehova,
motero kuti amamutumikira Iye,
amakonda dzina la Yehova,
amamugwirira ntchito,
komanso kusunga Sabata osaliyipitsa
ndi kusunga bwino pangano langa,
7 amenewa Ine ndidzawafikitsa ku phiri langa lopatulika,
ndidzawapatsa chimwemwe m’nyumba yanga ya mapemphero.
Zopereka zawo zopsereza ndi nsembe zawo
ndidzazilandira pa guwa langa la nsembe.
Paja nyumba yanga idzatchedwa
nyumba ya mapemphero ya anthu a mitundu yonse.”
8 Ambuye Yehova, amene amasonkhanitsa
Aisraeli onse ali ku ukapolo akunena kuti,
“Ndidzasonkhanitsano anthu ena
kuwonjezera amene anasonkhana kale.”

*Mulungu Adzazula Anthu Oyipa*

9 Bwerani, inu zirombo zonse zakuthengo,
inu nonse zirombo zam’nkhalango bwerani mudzadye!
10 Atsogoleri onse a Israeli ndi akhungu,
onse ndi opanda nzeru;
onse ndi agalu opanda mawu,
samatha kuwuwa:
amagona pansi n’kumalota
amakonda kugona tulo.
11 Ali ngati agalu amene ali ndi njala yayikulu;
sakhuta konse.
Abusa nawonso samvetsa zinthu;
onse amachita monga akufunira,
aliyense amafunafuna zomupindulitsa iye mwini.

12 Aliyense amafuwulira mnzake kuti, “Bwera, tiye timwe vinyo!
Tiyeni timwe mowa mpaka kukhuta!
Mawa lidzakhala ngati leroli,
kapena kuposa lero lino.”

# 57

1 Anthu olungama amafa,
ndipo palibe amene amalingalira mu mtima mwake;
anthu odzipereka amatengedwa,
ndipo palibe amene amamvetsa chifukwa chake.
Anthu olungama amatengedwa
kuti tsoka lisawagwere.
2 Iwo amene amakhala moyo wolungama
amafa mwamtendere;
amapeza mpumulo pamene agona mu imfa.

3 “Bwerani kuno, anthu ochita zoyipa,
inu muli ngati zidzukulu za mkazi wachigololo ndi wadama!
4 Kodi inu mukuseka yani?
Kodi mukumunena ndani
ndi kupotoza pakamwa panu?
Kodi inu si ana owukira,
zidzukulu za anthu abodza?
5 Inu mumapembedza mafano pamene mumalobodoka ndi zilakolako zanu pakati pa mitengo ya thundu,
ndiponso pa tsinde pa mtengo uliwonse wa nthambi zambiri.
Mumapereka ana anu ngati nsembe mu zigwa
ndiponso m’ming’alu ya m’matanthwe.
6 Mafano a pakati pa miyala yosalala ya mu zigwa ndiye chuma chanu.
Inde, ndiye gawo lanu.
Mumapereka chopereka cha chakumwa kwa mafanowo,
ndipo mumaperekanso chopereka cha chakudya.
Kodi zimenezi
zingandichititse kuti ndikukomereni mtima?
7 Inu munayiwala bedi lanu pa phiri lalitali ndi looneka kutali.
Mumapita kumeneko kukapereka nsembe zanu.
8 M’nyumba mwanu mwayika
mafano kuseri kwa zitseko ndiponso pa mphuthu.
Mwandisiya Ine, mwavula zovala zanu.
Bedi lanu mwalikulitsa ndipo mwakwera ndi zibwenzi zanu,
ndiye mwazilipira kuti mugone nazo.
Kumene mwakwaniritsa zilakolako zanu zoyipa.
9 Mumapita kukapembedza fano la Moleki mutatenga mafuta
ndi zonunkhira zochuluka.
Munachita kutumiza akazembe anu kutali;
inu ngakhale munapita ku manda kwenikweniko!
10 Inu mumatopa ndi maulendo anu,
koma simunathe kunena kuti, ‘N’zopanda phindu.’
Munapezako kumeneko zokhumba zanu
n’chifukwa chake simunalefuke.

11 “Kodi ndani amene mwachita naye mantha ndi kumuopa,
kotero kuti mwakhala mukundinamiza,

ndipo Ine simundikumbukira n'komwe,
kapena kuganizirapo m'mitima yanu za Ine?
Kodi mwaleka kundiopa chifukwa choti
ndakhala chete nthawi yayitali?
12 Koma ndaonetsa poyera ntchito zanu zomwe mumati n'zolungama,
ndi mafano anu kuti n'zosathandiza.
13 Pamene mufuwula kupempha thandizo,
mafano anu amene munasonkhanitsawo ndiyetu akupulumutseni!
Mphepo idzanyamula mafano anu onsewo,
mpweya chabe udzawulutsa mafanowo.
Koma munthu amene amadalira ine
adzalandira dziko lokhalamo.
Phiri langa lopatulika lidzakhala lakelake."

### *Mpumulo kwa Anthu Osweka Mtima*

14 Ndipo panamveka mawu akuti,
"Undani, undani, konzani msewu!
Chotsani zotchinga pa njira yoyendamo anthu anga."
15 Pakuti Iye amene ali Wamkulu ndi Wopambanazonse,
amene alipo nthawi zonse, amene dzina lake ndi Woyerayo,
akunena kuti, "Ndimakhala pamalo aulemu ndi opatulika,
koma ndimakhalanso ndi munthu wodzichepetsa ndi wosweka mtima
kuti odzichepetsawo ndiwalimbitse
ndi kuwachotsa mantha osweka mtima.
16 Sindidzawatsutsa anthu mpaka muyaya
kapena kuwapsera mtima nthawi zonse,
popeza kuti ndinalenga anthu anga
ndi kuwapatsa mpweya wamoyo.
17 Ine ndinakwiya kwambiri chifukwa cha tchimo lawo ladyera;
ndinawalanga ndi kuwafulatira mokwiya,
koma iwo anapitiririrabe kuchita ntchito zawo zoyipa.
18 Ndaona zochita zawo, komabe ndidzawachiritsa;
kuwapumulitsa ndi kuwapatsa mtendere,
19 anthu olira a mu Israeli adzanditamanda ndi milomo yawo.
Anthu amene ali kutali ndi apafupi pomwe ndidzawapatsa mtendere,"
"Ndipo ndidzawachiritsa."
Akutero Yehova.
20 Koma anthu oyipa ali ngati nyanja yowinduka,
yosatha kukhala bata,
mafunde ake amaponya matope ndi ndere.
21 "Palibe mtendere kwa oyipa," akutero Mulungu wanga.

## 58

### *Kusala Kwenikweni*

1 "Fuwula kwambiri, usaleke.
Mawu ako amveke ngati lipenga.
Uwawuze anthu anga za kulakwa kwawo;
uwuze nyumba ya Yakobo za machimo awo.
2 Pakuti tsiku ndi tsiku amafunafuna Ine;
amaoneka ngati a chidwi chofuna kudziwa zimene ndimafuna,
kukhala ngati kuti ndi dziko limene limachita zolondola
ndipo silinasiye zolamulira za Mulungu wake.

Amandipempha kuti ndigamule mlandu wawo mwachilungamo
ndipo amaonetsa chidwi chofuna kukhala pafupi ndi Mulungu.
3 Anthu akufunsa kuti, 'Chifukwa chiyani ife tasala
kudya pamene Inu simukulabadirapo?
Kodi ife tavutikiranji n'kudzichepetsa
pamene Inu simunasamalepo?' "

Yehova akuti, "Komatu tsiku lanu losala kudya, mumachita zinthu zokukondweretsani,
ndipo mumazunza antchito anu onse.
4 Mumati uku mukusala kudya, uku mukukangana ndi kumenyana,
mpaka kumenyana ndi nkhonya zopweteka.
Kusala kudya mukuchitiramu musayembekezere kuti mawu anu amveka kumwamba.
5 Kodi kusala kudya kumene ndimakufuna Ine n'kumeneku,
kungokhala tsiku loti munthu adzichepetse basi?
Kodi ndi tsiku loti munthu angowerama pansi ngati bango
ndi kumayala ziguduli n'kuthirapo phulusa n'kugonapo?
Kodi ndiye mumati kusala kudya kumeneko,
tsiku lokondweretsa Yehova?

6 "Kodi si uku kusala kudya kumene Ine ndimakufuna:
Kumasula maunyolo ozunzizira anthu
ndi kumasula zingwe za goli,
kupereka ufulu kwa oponderezedwa
ndi kuphwanya goli lililonse?
7 Anthu anjala kodi mwawagawira chakudya chanu?
Osowa ndi ongoyendayenda,
kodi mwawapatsa malo ogona?
Munthu wausiwa kodi mwamupatsa chovala?
8 Mukatero chipulumutso chanu chidzabwera ngati m'bandakucha,
ndipo mabala anu adzachira msangamsanga;
chilungamo chanu chidzakutsogolerani
ndipo ulemerero wa Yehova udzakhala chokutchinjirizani kumbuyo kwanu.
9 Mukamadzapemphera Yehova adzakuyankhani;
mukadzapempha thandizo, Iye adzati: Ine ndili pano.

"Ngati muleka kuzunza anzanu,
ngati musiya kuloza chala ndiponso kunena zoyipa za anzanu.
10 Ndipo ngati mudyetsa anthu anjala,
ndi kuthandiza anthu oponderezedwa,
pamenepo kuwala kwanu kudzaonekera mu mdima,
ndipo usiku wanu udzakhala ngati usana.
11 Yehova adzakutsogolerani nthawi zonse;
adzakwaniritsa zosowa zanu m'dziko long'alukang'aluka dzuwa
ndipo adzalimbitsa matupi anu.
Mudzakhala ngati dimba la madzi ambiri,
ngati kasupe amene madzi ake saphwa.
12 Anthu ako adzamanganso nyumba zimene zakhala mabwinja nthawi yayitali,
ndipo adzamanganso pa maziko akalekale;
inu mudzatchedwa okonza makoma opasuka.

Anthu okonza misewu ndi nyumba zake.

13 “Muzisunga osaphwanya Sabata;
musamachite zimene mukufuna pa masiku anga opatulika,
tsiku la Sabata lizikhala tsiku lachisangalalo.
Tsiku lopatulika la Yehova muzililemekeza
posayenda m’njira zanu,
kapena kuchita zimene mukufuna ndi kuyankhula zopandapake,
14 mukatero mudzapeza chimwemwe mwa Yehova,
ndipo ndidzakukwezani ndi kukupambanitsani pa dziko lonse lapansi.
Mudzadyerera dziko limene ndinapatsa Yakobo kholo lanu.”
Yehova wayankhula ndi pakamwa pake.

# 59

*Tchimo, Kuvomereza ndi Chipulumutso*

1 Taonani, mkono wa Yehova si waufupi kuti sungathe kupulumutsa,
kapena khutu lake kuti ndilogontha kuti sangamve.
2 Koma zoyipa zanu zakulekanitsani
ndi Mulungu wanu;
ndipo wakufulatirani chifukwa cha machimo anu,
kotero Iye sadzamva.
3 Pakuti manja anu ali psuu ndi magazi.
Munayipitsa zala zanu ndi zamphulupulu.
Pakamwa panu payankhula zabodza,
ndipo lilime lanu lanena zinthu zoyipa.
4 Palibe amene akuyimba mnzake mlandu molungama,
palibe amene akupita ku mlandu moona mtima.
Iwo amadalira mawu opanda pake ndipo amayankhula mabodza;
amalingalira za mphulupulu ndipo amachita zoyipa.
5 Iwo amayikira mazira a mamba
ndipo amaluka ukonde wakangawude.
Aliyense amene adzadya mazira awo adzafa,
ndipo ngati dzira limodzi lasweka limatulutsa mphiri.
6 Ukonde wawo wa kangawude sangawuvale ngati chovala;
ndipo chimene apangacho sangachifunde.
Ntchito zawo ndi zoyipa,
ndipo amakonda kuchita zandewu ndi manja awo.
7 Amathamangira kukachita zoyipa;
sachedwa kupha anthu osalakwa.
Maganizo awo ndi maganizo oyipa;
kulikonse kumene amapita amasiyako bwinja ndi chiwonongeko.
8 Iwo sadziwa kuchita za mtendere;
zonse zimene amachita n’zopanda chilungamo.
Njira zawo zonse n’zokhotakhota;
aliyense oyenda m’njira zimenezo sadzapeza mtendere.

9 Anthu akuti, “Chifukwa cha zimenezi chilungamo chatitalikira;
ndipo chipulumutso sichitifikira.
Timafunafuna kuwala koma timangopeza mdima okhaokha;
tinayembekezera kuyera koma timayenda mu mdima wandiweyani.
10 Timapapasapapasa khoma ngati munthu wosaona,

kuyang'anayang'ana njira ngati anthu opanda maso.
Timapunthwa dzuwa lili paliwombo ngati kuti ndi usiku;
timakhala pansi mu mdima ngati anthu akufa.
11 Tonse timabangula ngati zimbalangondo:
Timalira modandaula ngati nkhunda.
Tinayembekezera kuweruza kolungama; koma sitikupeza.
Timayembekezera chipulumutso koma chimakhala nafe kutali."

12 Pakuti zolakwa zathu n'zochuluka pamaso panu,
ndipo machimo athu akutsutsana nafe.
Zolakwa zathu zili ndi ife nthawi zonse
ndipo tikuvomereza machimo athu:
13 Tawukira ndi kumukana Yehova.
Tafulatira Mulungu wathu,
pa kupondereza anzathu ndi kupandukira Yehova,
ndi pa kuyankhula mabodza amene tawaganiza m'mitima mwathu.
14 Motero kuweruza kolungama kwalekeka
ndipo choonadi chili kutali ndi ife;
kukhulupirika sikukupezekanso m'mabwalo a milandu,
ndipo kuona mtima sikukupezekanso m'menemo.
15 Choonadi sichikupezeka kumeneko,
ndipo wina akakana kuchita nawo zoyipa amapeza mavuto.

Yehova anaziona zimenezi ndipo zinamunyansa
kuti panalibe chiweruzo cholungama.
16 Yehova anaona kuti panalibe ndi mmodzi yemwe,
Iye anadabwa kuti panalibe ndi mmodzi yemwe woti n'kupembedzera;
Choncho mphamvu zake zomwe zinamuthandiza,
ndipo anadzilimbitsa ndi kulungama kwake;
17 Iye anavala chilungamo ngati chovala chachitsulo chapachifuwa,
ndipo kumutu kwake amavala chipewa chachipulumutso;
anavala kulipsira ngati chovala
ndipo anadzikuta ndi mkwiyo ngati chofunda.
18 Iye adzawabwezera chilango adani a anthu ake
molingana ndi zimene anachita,
adzaonetsa ukali kwa adani ake
ndi kubwezera chilango odana naye.
Adzalanga ngakhale okhala mayiko akutali.
19 Choncho akadzabwera ngati madzi
oyendetsedwa ndi mphepo yamphamvu yamkuntho.
Anthu onse kuyambira kumadzulo mpaka kummawa
adzaopa dzina la Yehova ndi ulemerero wake.

20 "Mpulumutsi adzabwera ku Ziyoni
kudzapulumutsa anthu a fuko la Yakobo amene analapa machimo awo,"
akutero Yehova.
21 Yehova akuti, "Kunena za pangano lake ndi iwo, Mzimu wanga
umene uli pa inu, ndiponso mawu anga amene ndayika m'kamwa mwanu
sadzachoka m'kamwa mwanu, kapena kuchoka m'kamwa mwa ana

anu, kapena m'kamwa mwa zidzukulu zawo kuyambira tsopano mpaka kalekale,"
akutero Yehova.

# 60

*Ulemerero wa Ziyoni*

1 "Dzuka, wala, pakuti kuwala kwako kwafika,
ndipo ulemerero wa Yehova wakuwalira.
2 Taona, mdima waphimba dziko lapansi
ndipo mdima wandiweyani wagwa pa anthu a mitundu ina,
koma Yehova adzakuwalira iwe,
ndipo ulemerero wake udzaoneka pa iwe.
3 Mitundu ya anthu idzatsata kuwunika kwako
ndipo mafumu adzalondola kunyezimira kwa m'bandakucha wako.

4 "Tukula maso ako, yang'anayang'ana ndipo ona zimene zikuchitika.
Onse akusonkhana ndipo akubwera kwa iwe;
ana ako a amuna akubwera kuchokera kutali
ndipo ana ako aakazi anyamulidwa m'manja.
5 Ukadzaona zimenezi udzasangalala kwambiri,
mtima wako udzalumpha ndi kudzaza ndi chimwemwe;
chuma chakunyanja chidzabwera kwa iwe
chuma cha mitundu ya anthu chidzabwera kwa iwe.
6 Gulu la ngamira lidzaphimba dziko lako,
ngamira zing'onozing'ono zidzachokera ku Midiyani ndi ku Efai.
Ndipo onse a ku Seba adzabwera
atanyamula golide ndi lubani
uku akutamanda Yehova.
7 Ziweto zonse za ku Kedara adzazisonkhanitsa kwa inu,
nkhosa zazimuna za ku Nabayoti zidzakutumikirani;
zidzalandiridwa monga chopereka pa guwa langa la nsembe,
ndipo ndidzakongoletsa Nyumba yanga.

8 "Kodi ndi zayani izo zikuwuluka ngati mitambo,
ngati kapena nkhunda zobwerera ku zisa zawo?
9 Ndithu, izi ndi sitima za pa madzi zochokera ku mayiko akutali;
patsogolo pali sitima zapamadzi za ku Tarisisi,
zikubweretsa ana ako ochokera kutali,
pamodzi ndi siliva wawo ndi golide wawo,
kudzalemekeza Yehova Mulungu wako,
Woyerayo wa Israeli,
pakuti Iye wakuvekani inu ulemerero.

10 "Alendo adzamanganso malinga ako,
ndipo mafumu awo adzakutumikira.
Ngakhale ndinakukantha ndili wokwiya,
koma tsopano ndidzakukomera mtima ndikukuchitira chifundo.
11 Zipata zako zidzakhala zotsekula nthawi zonse,
sadzazitseka nthawi zonse, usana ndi usiku,
kotero anthu adzabwera kwa iwe ndi chuma chawo,
akuyenda pa mdipiti mafumu awo ali patsogolo.
12 Pakuti mtundu wa anthu ndi mafumu amene sakutumikira iwe;

adzawonongeka kotheratu.

13 “Adzabwera nayo kwa iwe mitengo ya payini,
mkuyu ndi naphini imene ili m’nkhalango ya Lebanoni
kuti adzakongoletsere malo a nyumba yanga yopatulika;
ndipo ndidzalemekeza malo amene Ine ndimapondapo.
14 Ana aja amene anakuzunzani adzabwera ndipo adzakugwadirani;
onse amene anakunyozani adzagwada pansi pa mapazi anu.
Ndipo adzakutchani kuti Mzinda wa Yehova;
Ziyoni mzinda wa Woyerayo wa Israeli.

15 “Ngakhale anthu anakusiya nadana nawe,
koma Ine ndidzakukuza mpaka muyaya,
ndipo udzakhala malo a chimwemwe
cha anthu amibado yonse.
16 Udzamwa mkaka wa mitundu ya anthu
ndi kuleredwa pa maere aufumu,
motero udzadziwa kuti Ine Yehova, ndine Mpulumutsi wako,
Momboli wako ndiye Wamphamvu wa Yakobo.
17 Ndidzakupatsa golide m’malo mwa mkuwa,
ndi siliva m’malo mwa chitsulo.
Ndidzakupatsa mkuwa m’malo mwa thabwa
ndi chitsulo m’malo mwa miyala.
Olamulira ako adzakhala a mtendere.
Ndidzasandutsa okulamulira kuti akhale achilungamo.
18 Ziwawa sizidzamvekanso m’dziko lako,
bwinja kapena chiwonongeko sizidzapezeka m’dziko lako,
ndidzakhala malinga ako okuteteza
ndipo udzanditamanda.
19 Sipadzakhala dzuwa kuti likuwunikire,
kapena mwezi kuti uwunikire usiku,
pakuti Yehova ndiye adzakhale kuwunika kwako kwa muyaya,
ndipo Mulungu wako adzakhala ulemerero wako.
20 Dzuwa lako silidzalowanso,
ndipo mwezi wako sudzazimiriranso;
Yehova adzakhala kuwunika kwako kwamuyaya,
ndipo masiku a mavuto ako adzatha.
21 Ndipo anthu ako onse adzakhala olungama
ndipo dzikolo lidzakhala lawo mpaka muyaya.
Iwo ndi mphukira imene Ine ndayidzala,
ntchito ya manja anga,
kuti aonetse ulemerero wanga.
22 Kabanja kakang’ono kadzasanduka fuko,
kafuko kakang’ono kudzasanduka mtundu wamphamvu.
Ine ndine Yehova,
nthawi yake ikafika ndidzazichita zimenezi mofulumira.”

# 61

### *Uthenga Wabwino wa Yehova*

1 Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine,
chifukwa Yehova wandidzoza
kuti ndilalikire uthenga wabwino kwa anthu osauka.

Wandituma kuti ndikatonthoze anthu osweka mtima,
ndikalengeze kwa akapolo kuti alandire ufulu
ndiponso kuti ndikamasule a m'ndende.
2 Wanditumа kuti ndikalengeze nthawi imene Yehova adzapulumutsa anthu ake;
za tsiku limene Yehova adzalanga adani a anthu ake.
Wanditumа kuti ndikatonthoze olira.
3 Wanditumа kuti ndiwakonzere olira a ku Ziyoni,
nkhata ya maluwa yokongola
m'malo mwa phulusa,
ndiwapatse mafuta achikondwerero
m'malo mwa kulira.
Ndiwapatse chovala cha matamando
m'malo mwa mtima wopsinjika.
Ndipo iwo adzatchedwa mitengo ya thundu yamphamvu yachilungamo,
yoyidzala Yehova
kuti Iye mwini apezemo ulemerero wake.

4 Adzamanganso mabwinja akale a mzinda
ndipo malo amene anawonongeka kalekale aja adzakonzanso.
Adzakonzanso mizinda imene inapasuka,
imene yakhala yowonongeka kwa nthawi yayitali kwambiri.
5 Anthu achilendo adzakutumikirani; adzazidyetsa ziweto zanu;
iwo adzagwira ntchito m'minda yanu ya mpesa.
6 Ndipo inu mudzatchedwa ansembe a Yehova,
adzakutchulani kuti ndinu atumiki a Mulungu wathu.
Mudzadyerera chuma cha mitundu ya anthu,
ndipo mudzanyadira ulemu umene mwalandira.

7 Chifukwa manyazi awo anali owirikiza;
ndi kuti munalandira
chitonzo ndi kutukwana,
adzakondwera ndi cholowa chawo,
tsono adzalandira cholowa chawo cha chigawo cha dziko mowirikiza,
ndipo chimwemwe chamuyaya chidzakhala chawo.

8 "Pakuti Ine Yehova, ndimakonda chilungamo;
ndimadana ndi zakuba ndi zoyipa.
Anthu anga ndidzawapatsa mphotho mokhulupirika
ndikupangana nawo pangano losatha.
9 Ana awo adzakhala odziwika pakati pa mitundu ya anthu
ndipo adzukulu awo adzakhala otchuka pakati pa anthu a mitundu ina.
Aliyense wowaona adzazindikira
kuti ndi anthu amene Yehova wawadalitsa."

10 Ine ndikusangalala kwambiri chifukwa cha Yehova;
moyo wanga ukukondwera chifukwa cha Mulungu wanga.
Pakuti Iye wandiveka zovala zachipulumutso,
ndipo wandiveka mkanjo wachilungamo.
Zili ngati mkwati wovala nkhata ya maluwa m'khosi mwake,
ndiponso ngati mkwatibwi wovala mikanda yamtengowapatali.
11 Monga momwe nthaka imameretsa mbewu

ndiponso monga munda umakulitsa mbewu zimene anadzala,
momwemonso Ambuye Yehova adzaonetsa chilungamo ndi matamando
pamaso pa mitundu yonse ya anthu.

# 62

*Dzina Latsopano la Ziyoni*

1 Chifukwa chokonda Ziyoni sindidzakhala chete,
chifukwa chokonda Yerusalemu sindidzakhala chete,
mpaka chilungamo chake chitaoneka poyera ngati kuwala,
ndi chipulumutso chake chitaoneka ngati sakali yoyaka.
2 Mitundu ya anthu idzaona iwe utapambana pa nkhondo
ndipo mafumu onse adzaona ulemerero wako.
Adzakuyitanira dzina latsopano
limene adzakupatse ndi Yehova.
3 Udzakhala ngati chipewa chaulemerero m'dzanja la Yehova,
ndi ngati nduwira yaufumu m'dzanja la Mulungu wako.
4 Sadzakutchanso "Wosiyidwa,"
ndipo dziko lako silidzatchedwanso "Chipululu."
Koma dzina lako latsopano lidzakhala "Ndakondwera naye."
Ndipo dziko lako lidzatchedwa "Wokwatiwa."
Chifukwa Yehova akukondwera nawe,
ndipo adzakhala ngati mwamuna wa dziko lako.
5 Monga mnyamata amakwatira namwali,
momwenso mmisiri wodzakumanga adzakukwatira;
monga mkwati amakondwera ndi mkwatibwi,
chonchonso Mulungu adzakondwera nawe.

6 Iwe Yerusalemu, pa malinga ako ndayikapo alonda;
sadzakhala chete usana kapena usiku.
Inu amene mumakumbutsa Yehova za malonjezo ake
musapumule.
7 Musamupatse mpata wopuma mpaka atakhazikitsa Yerusalemu
kukhala mzinda umene dziko lapansi lidzawutamande.

8 Yehova analumbira atakweza dzanja lake.
Anati,
"Sindidzaperekanso tirigu wako
kuti akhale chakudya cha adani ako,
ndipo alendo sadzamwanso vinyo wako watsopano
pakuti unamuvutikira.
9 Koma amene amakakolola ndiwo amene adzadye buledi
ndi kutamanda Yehova,
ndipo amene amasonkhanitsa pamodzi mphesa ndiwo amene adzamwe vinyo
m'mabwalo a Nyumba yanga."

10 Tulukani, dutsani pa zipata!
Konzerani anthu njira.
Lambulani, lambulani msewu waukulu!
Chotsani miyala.
Kwezani mbendera kuti mitundu ya anthu izione.

11 Yehova walengeza
ku dziko lonse lapansi kuti,
Awuzeni anthu a ku Yerusalemu kuti,
“Taonani, chipulumutso chanu chikubwera;
Yehova akubwera ndi mphotho yake
akubwera nazo zokuyenerani.”
12 Iwo adzatchedwa Anthu Opatulika,
owomboledwa a Yehova;
ndipo adzakutchani “Okondwa a Yehova”
“Mzinda umene Yehova sanawusiye.”

# 63

*Yehova Agonjetsa Anthu a Mitundu Ina*

1 Kodi ndani uyo akubwera kuchokera ku Edomu,
atavala zovala za ku Bozira za madontho ofiira?
Kodi uyu ndani, amene wavala zovala zokongola,
akuyenda mwa mphamvu zake?

“Ndi Ineyo, woyankhula zachilungamo
ndiponso wamphamvu zopulumutsa.”

2 Nanga bwanji zovala zanu zili psuu,
ngati za munthu wofinya mphesa?

3 “Ndapondereza ndekha anthu a mitundu ina ngati mphesa,
palibe ndi mmodzi yemwe anali nane.
Ndinawapondereza ndili wokwiya
ndipo ndinawapondereza ndili ndi ukali;
magazi awo anadothera pa zovala zanga,
ndipo zovala zanga zonse zinathimbirira.
4 Pakuti ndinatsimikiza mu mtima mwanga kuti lafika tsiku lolipsira anthu anga;
ndipo chaka cha kuwomboledwa kwanga chafika.
5 Ndinayang’ana ndipo panalibe munthu wondithandiza.
Ndinadabwa kwambiri kuti panalibe wondichirikiza;
choncho ndinapambana ndi mphamvu zanga,
ndipo mkwiyo wanga unandilimbitsa.
6 Ndinapondereza mitundu ya anthu ndili wokwiya;
ndipo ndinawasakaza
ndipo ndinathira magazi awo pansi.”

*Matamando ndi Pemphero*

7 Ndidzafotokoza za kukoma mtima kwa Yehova,
ntchito zimene Iye ayenera kutamandidwa.
Ndidzatamanda Yehova chifukwa cha zonse zimene watichitira.
Inde, mwa chifundo ndi kukoma mtima kwake
Yehova wachitira nyumba ya Israeli
zinthu zabwino zambiri.
8 Yehova anati, “Ndithu awa ndi anthu anga,
ana anga amene sadzandinyenga Ine.”
Choncho anawapulumutsa.
9 Iyenso anasautsidwa m’masautso awo onse,

ndipo mngelo wochokera kwa Iye anawapulumutsa.
Mwa chikondi ndi chifundo chake iye anawapulumutsa,
anawanyamula ndikuwatenga
kuyambira kale lomwe.
10 Komabe iwo anawukira
ndi kumvetsa chisoni Mzimu Woyera.
Motero Yehova anatembenuka nakhala mdani wawo
ndipo Iye mwini anamenyana nawo.

11 Pamenepo anthu ake anakumbukira masiku amakedzana,
masiku a Mose mtumiki wake;
ndipo anafunsa kuti, "Ali kuti Yehova amene anawawolotsa pa nyanja,
pamodzi ndi Mose m'busa wawo?
Ali kuti Iye amene anayika
Mzimu Woyera pakati pawo?
12 Ali kuti amene anachita zinthu zodabwitsa
ndi mphamvu zake zazikulu kudzera mwa Mose?
Ali kuti amene anagawa madzi pa nyanja anthu ake akuona,
kuti dzina lake limveke mpaka muyaya,
13 amene anawayendetsa pa nyanja yozama?
Monga kavalo woyendayenda m'chipululu,
iwo sanapunthwe;
14 Mzimu Woyera unawapumulitsa
ngati mmene ng'ombe zimapumulira.
Umu ndi mmene Inu munatsogolera anthu anu
kuti dzina lanu lilemekezeke."

15 Inu Yehova amene muli kumwambako, pa mpando wanu wolemekezeka,
wopatulika ndi waulemerero, tiyang'aneni ife.
Kodi changu chanu ndi mphamvu zanu zili kuti?
Simukutionetsanso kukoma mtima kwanu ndi chifundo chanu.
16 Koma Inu ndinu Atate athu,
ngakhale Abrahamu satidziwa
kapena Israeli kutivomereza ife;
Inu Yehova, ndinu Atate athu,
kuyambira kale dzina lanu ndinu Mpulumutsi wathu.
17 Chifukwa chiyani, Inu Yehova, mukutisocheretsa pa njira zanu?
Bwanji mukutilola kuti tikhale owuma mitima kotero kuti sitikukuopaninso?
Bwererani chifukwa cha atumiki anu;
mafuko a anthu amene ali cholowa chanu.
18 Anthu anu atangokhala pa malo anu opatulika pa kanthawi kochepa,
adani athu anasakaza malo anu opatulika.
19 Ife tili ngati anthu amene
simunawalamulirepo
ngati iwo amene sanakhalepo anthu anu.

# 64

1 Inu Yehova, bwanji mukanangong'amba mlengalenga ndi kutsika pansi,
kuti mapiri agwedezeke pamaso panu!
2 Monga momwe moto umatenthera tchire
ndiponso kuwiritsa madzi,

tsikani kuti adani anu adziwe dzina lanu,
ndiponso kuti mitundu ya anthu injenjemere pamaso panu.
3 Pakuti nthawi ina pamene munatsika munachita zinthu zoopsa zimene sitinaziyembekezere,
ndipo mapiri anagwedezeka pamaso panu.
4 Chikhalire palibe ndi mmodzi yemwe anamvapo
kapena kuona
Mulungu wina wonga Inu,
amene amachitira zinthu zotere amene amadikira pa Iye.
5 Inu mumabwera kudzathandiza onse amene amakondwera pochita zolungama,
amene amakumbukira njira zanu.
Koma Inu munakwiya,
ife tinapitiriza kuchimwa.
Kodi nanga tingapulumutsidwe bwanji?
6 Tonsefe takhala ngati anthu amene ndi odetsedwa,
ndipo ntchito zathu zili ngati sanza za msambo;
tonse tafota ngati tsamba,
ndipo machimo athu akutiwuluzira kutali ngati mphepo.
7 Palibe amene amapemphera kwa Inu
kutekeseka kuti apemphe chithandizo kwa Inu;
pakuti mwatifulatira
ndi kutisiya chifukwa cha machimo athu.

8 Komabe, Inu Yehova ndinu Atate athu.
Ife ndife chowumba, Inu ndinu wowumba;
ife tonse ndi ntchito ya manja anu.
9 Inu Yehova, musatikwiyire kopitirira muyeso
musakumbukire machimo athu mpaka muyaya.
Chonde, mutiganizire, ife tikupempha,
pakuti tonsefe ndi anthu anu.
10 Mizinda yanu yopatulika yasanduka chipululu;
ngakhaletu Ziyoni wasanduka chipululu, Yerusalemu ndi wamasiye.
11 Nyumba yanu yopatulika ndi yaulemu, kumene makolo athu ankakutamandani,
yatenthedwa ndi moto
ndipo malo onse amene tinkawakonda asanduka bwinja.
12 Inu Yehova, zonse zachitikazi, kodi mungokhala osatithandiza?
Kodi mudzapitirizabe kukhala chete ndi kutilangabe mopitirira muyeso?

# 65

*Chiweruzo ndi Chipulumutso*

1 "Ndinali wokonzeka kumva mapemphero a amene sankandipempha kanthu;
ndipo ndinalola kuti anthu amene ankandifunafuna kuti andipeze.
Kwa mtundu wa anthu umene sunkapempha chithandizo kwa Ine,
ndinati, 'Ine ndili pano, Ine ndili pano.'
2 Tsiku lonse ndatambasulira manja anga
anthu owukira aja,
amene amachita zoyipa,
natsatira zokhumba zawo.

3 Ndatambasulira manja anga anthu aja amene nthawi zonse amandikwiyitsa
mopanda manyazi.
Iwo amapereka nsembe m'minda
ndi kufukiza lubani pa maguwa ansembe a njerwa.
4 Amakatandala ku manda
ndipo amakachezera usiku wonse kumalo obisika.
Amadya nyama ya nkhumba,
ndipo m'miphika mwawo muli msunzi wa nyama yodetsedwa.
5 Amawuza ena kuti, 'Khala patali usandiyandikire,
chifukwa ungatengere kupatulika kwanga!'
Ukali wanga pa anthu otere uli ngati utsi mphuno zanga,
ngati moto umene umayaka tsiku lonse.

6 "Taonani, ndatsimikiza kale mlandu ndi chilango chawo;
sindidzakhala chete koma ndidzawalanga kwathunthu
chifukwa cha machimo awo
7 ndi a makolo awo,"
akutero Yehova.
"Chifukwa anapereka nsembe zopsereza pa mapiri
ndi kundinyoza Ine pa zitunda zawo,
Ine ndidzawalanga kwathunthu potsata
zimene anachita kale."
8 Yehova akuti,
"Pamene madzi akanapezeka mu phava la mphesa
ndipo anthu amati, 'Musawononge phavalo,
popeza madzi ena abwino akanalimobe m'phavalo,'
Inenso chifukwa cha mtumiki wanga;
sindidzawononga onse.
9 Ndidzatulutsa zidzukulu m'banja la Yakobo,
ndipo a banja la Yuda adzalandira mapiri anga ngati cholowa chawo.
Anthu anga osankhidwa adzalandira zimenezi,
ndipo atumiki anga adzakhala kumeneko.
10 Chigwa cha Saroni chidzakhala kodyetserako nkhosa,
ndipo chigwa cha Akori chidzakhala malo opumirako ng'ombe
kwa anthu anga ondifunafuna Ine.

11 "Koma inu amene mumasiya Yehova
ndi kuyiwala phiri langa lopatulika,
amene munamukonzera Gadi chakudya
ndi kuthirira Meni chakumwa,
12 ndidzakuperekani ku lupanga ngati nsembe,
ndipo nonse mudzaphedwa;
chifukwa simunayankhe pamene ndinakuyitanani,
ndinayankhula koma simunamvere.
Munachita zoyipa pamaso panga
ndipo munasankha kuchita zoyipa zomwe sindikondwera nazo."
13 N'chifukwa chake Ambuye Yehova akuti,
"Atumiki anga adzadya,
koma inu mudzakhala ndi njala;
atumiki anga adzamwa,
koma inu mudzakhala ndi ludzu;
atumiki anga adzakondwa,

koma inu mudzakhala ndi manyazi.
14 Atumiki anga adzayimba
mosangalala,
koma inu mudzalira kwambiri
chifukwa chovutika mu mtima
ndipo mudzalira mofuwula chifukwa mudzamva kuwawa mu mtima.
15 Anthu anga osankhidwa
adzatchula dzina lanu potemberera.
Ambuye Yehova adzakuphani,
koma atumiki ake adzawapatsa dzina lina.
16 Aliyense wopempha dalitso m'dzikomo
adzachita zimenezo kwa Mulungu woona;
ndipo aliyense wochita malumbiro m'dzikomo
adzalumbira mwa Mulungu woona.
Pakuti mavuto akale adzayiwalika
ndipo adzachotsedwa pamaso panga.

### *Chilengedwe Chatsopano*

17 "Taonani, ndikulenga
mlengalenga mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano.
Zinthu zakale sizidzakumbukika,
zidzayiwalika kotheratu.
18 Koma inu mukhale osangalala ndi okondwa mpaka muyaya
chifukwa cha zimene ndikulenga,
pakuti ndikulenga Yerusalemu kukhala malo wosangalatsa
ndipo anthu ake adzakhala achimwemwe.
19 Ine ndidzakondwa chifuwa cha Yerusalemu
ndipo ndidzasangalala chifukwa cha anthu anga.
Kumeneko sikudzamvekanso kulira
ndi mfuwu wodandaula.

20 "Ana sadzafa ali akhanda
ndipo nkhalamba zonse zidzakwaniritsa zaka zawo zonse.
Wamng'ono mwa iwo
adzafa ali ndi zaka 100.
Amene adzalephere kufika zaka 100
adzatengedwa kukhala
wotembereredwa.
21 Anthu adzamanga nyumba ndi kukhalamo,
adzadzala mpesa ndipo adzadya zipatso zake.
22 Sadzamanganso nyumba anthu ena n'kukhalamo,
kapena kudzala ndi ena n'kudya.
Pakuti anthu anga adzakhala ndi moyo
wautali ngati mitengo.
Osankhidwa anga adzakondwera ndi ntchito
ya manja awo nthawi yayitali.
23 Sadzagwira ntchito pachabe
kapena kubereka ana kuti aone tsoka;
chifukwa adzakhala anthu odalitsidwa ndi Yehova,
iwowo pamodzi ndi adzukulu awo omwe.
24 Ndidzawayankha ngakhale asanathe n'kupempha komwe.
Pamene akuyankhula kumene Ine ndidzakhala nditamva kale.
25 M'mbulu ndi mwana wankhosa wamkazi zidzadyera pamodzi.

Mkango udzadya udzu monga ng'ombe,
koma fumbi ndiye chidzakhale chakudya cha njoka.
Pa phiri langa lopatulika sipadzakhala
chinthu chopweteka kapena chowononga,"
akutero Yehova.

# 66

*Chiweruzo ndi Chiyembekezo*

1 Yehova akuti,
"Kumwamba ndi mpando wanga waufumu
ndipo dziko lapansi ndilo chopondapo mapazi anga.
Tsono nyumba ili kuti yomwe mundimangire,
ndipo malo ali kuti amene inu mungandikonzere kuti ndizipumuliramo?
2 Kodi si manja anga amene anapanga zinthu zonsezi,
motero zonsezi ndi zanga?"
Akutero Yehova.

"Koma munthu amene ndimakondwera naye ndi uyu:
amene ali wodzichepetsa ndi wosweka mtima,
ndipo amamvera mawu anga.
3 Koma aliyense amene amapereka nsembe ng'ombe yayimuna
amaphanso munthu,
ndipo aliyense amene amapereka mwana wankhosa,
amaphanso galu.
Aliyense amene amapereka nsembe chopereka cha chakudya
amaperekanso magazi a nkhumba.
Ndipo amene amafukiza lubani pa guwa lansembe la chikumbutso
amapembedzanso fano.
Popeza iwo asankha njira zawozawo,
ndiponso kusangalatsidwa ndi zonyansa zawo.
4 Inenso ndawasankhira chilango chowawa
ndipo ndidzabweretsa pa iwo zimene amaziopa zija.
Pakuti pamene ndinawayitana palibe amene anayankha,
pamene ndinayankhula palibe amene anatchera khutu.
Anachita zoyipa pamaso panga
ndi kusankha kuchita zimene zimandinyansa zija."

5 Imvani mawu a Yehova,
inu amene mumanjenjemera ndi mawu ake:
"Abale anu amene amakudani,
ndi kukuchotsani pakati pawo chifukwa cha dzina langa, amanena kuti,
'Yehova alemekezeke
kuti ife tione chimwemwe chanu!'
Koma ndi iwowo amene adzachite manyazi.
6 Imvani mfuwu mu mzinda,
imvani phokoso m'Nyumba ya Mulungu!
Limenelo ndi liwu la Yehova,
kulanga adani ake onse.

7 "Mzinda uli ngati amayi apakati amene asanayambe kumva zowawa
wachira kale;

asanayambe kumva ululu,
wabala kale mwana wamwamuna.
8 Ndani anamvapo zinthu zoterezi?
Ndani anazionapo zinthu zoterezi?
Kodi dziko n'kupangika tsiku limodzi,
kapena mtundu wa anthu n'kubadwa tsiku limodzi?
Komatu Ziyoni atangoyamba kumva zowawa
nthawi yomweyo anabereka ana ake.
9 Kodi Ine ndingangofikitsa amayi apakati mpaka nthawi yake yochira,
koma osalola kuti abaledi mwana?" akutero Yehova.
"Kodi ndingatseke mimba
pa nthawi yoti abeleke?" akutero Mulungu wako.
10 "Kondwera nayeni Yerusalemu ndipo musangalale chifukwa cha Iye,
inu nonse amene mumakonda Yerusalemu,
kondwera nayeni kwambiri,
nonse amene mumamulira.
11 Pakuti mudzagawana naye ulemerero wake
ngati kuyamwa ndi kukhuta mkaka wambiri
wa m'mawere
a chitonthozo chake."
12 Yehova akuti,
"Ndidzamupatsa mtendere ngati mtsinje wa madzi,
ndiponso chuma cha anthu a mitundu ina ngati mtsinje wosefukira.
Mudzakhala ngati mwana woyamwa amene amayi ake amunyamulira pambalipa,
kapena kumufungata pa miyendo yake.
13 Monga momwe amayi amasangalatsira mwana wawo,
moteronso Ine ndidzakusangalatsani;
ndipo mudzasangalala chifukwa cha Yerusalemu."

14 Mukadzaona zimenezi mitima yanu idzakondwera. Mudzabiriwira ngati udzu.
Zimenezi zidzakulimbikitsani ndi kukupatsani moyo wamphamvu.
Mudzadziwa kuti ndimathandiza amene amanditumikira
ndi kuti ndimakwiyira adani anga.
15 Taonani, Yehova akubwera ngati moto,
ndipo magaleta ake ali ngati kamvuluvulu;
Iye adzaonetsa mkwiyo wake nadzalanga adani ake
ndi malawi amoto.
16 Pakuti Yehova adzalanga anthu onse
ndi moto ndi lupanga,
Yehova adzapha anthu ambiri.

17 Yehova akuti, "Amene amadzipatula ndi kudziyeretsa okha kuti apite ku minda, ali ndi mtsogoleri awo, n'kumadya nyama ya nkhumba, mbewa ndi zinthu zina zonyansa, onsewa adzafera limodzi."

18 "Ndipo Ine, chifukwa cha zochita zawo ndi maganizo awo, ndili pafupi kubwera kudzasonkhanitsa mitundu yonse ya anthu ndi ziyankhulo zonse. Iwo adzabwera ndi kuona ulemerero wanga.

19 "Ndidzayika chizindikiro pakati pawo, ndipo ndidzatumiza ena mwa iwowa amene anapulumuka kuti apite kwa anthu a mitundu ina inu ku Tarisisi, ku Libiya ndi ku Ludi (akatswiri a mauta) ku Tubala ndi Grisi, ndi ku mayiko akutali a mbali mwa nyanja amene sanamvepo za mbiri yanga kapena kuona ulemerero wanga. Iwo adzalalika za ulemerero wanga

pakati pa anthu a mitundu ina. [20] Ndipo adzabwera nawo abale anu onse
ngati mphatso yopereka kwa Yehova kuchokera kwa anthu a mitundu
yonse. Iwo adzakwera nawo kupita ku Yerusalemu, phiri langa loyera
ku Yerusalemu monga nsembe kwa Yehova, atakwera akavalo, magaleta
ndi ngolo, ndi pa abulu ndi ngamira," akutero Yehova. "Adzabwera nawo
ngati momwe Aisraeli amabwerera ndi zopereka zachakudya ku Nyumba
ya Yehova mu ziwiya zoyeretsedwa monga mwa mwambo. [21] Ndipo
ndidzasankha ena mwa iwonso kukhala ansembe ndi Alevi," akutero
Yehova.

[22] "Monga momwe mlengalenga mwatsopano ndi dziko lapansi lat-
sopano zimene ndidzapanga zidzakhala mpaka muyaya pamaso panga,
ndi chonchonso dzina lanu ndi zidzukulu zanu zidzakhalire." Akutero
Yehova. [23] "Anthu a mitundu yonse adzabwera kudzandipembedza
ku Yerusalemu, pa chikondwerero chilichonse cha pokhala pa mwezi
watsopano ndi tsiku la Sabata lililonse," akutero Yehova. [24] "Akamachoka
adzaona mitembo ya anthu amene anandiwukira Ine. Mphutsi zawo
sizidzafa, kapena moto wawo sudzazimitsidwa. Anthu a mitundu ina
yonse powaona adzanyansidwa nawo."

# Yeremiya

1 Mawu a Yeremiya mwana wa Hilikiya, mmodzi mwa ansembe a ku
Anatoti, m'dziko la Benjamini. 2 Mawuwa Yehova anayankhula naye
m'chaka cha 13 cha ulamuliro wa Yosiya mwana wa Amoni mfumu ya
Yuda. 3 Yehova anayankhulanso naye pa nthawi yonse ya ulamuliro wa
Yehoyakimu mwana wa Yosiya mfumu ya Yuda, mpaka mwezi wachisanu wa chaka cha 11 cha ufumu wa Zedekiya mwana wa Yosiya mfumu ya Yuda, pamene anthu a ku Yerusalemu anapita ku ukapolo.

*Kuyitanidwa kwa Yeremiya*

4 Yehova anayankhula nane kuti,

5 "Ndisanakuwumbe m'mimba mwa amayi ako ndinali nditakudziwa kale,
iwe usanabadwe ndinali nditakupatula kale;
ndinakuyika kuti ukhale mneneri kwa anthu a mitundu yonse."

6 Ine ndinati, "Haa! Ambuye Yehova, ine sinditha kuyankhula; popeza ndikanali wamng'ono."

7 Koma Yehova anandiwuza kuti, "Usanene kuti, 'Ndikanali wamng'ono'
popeza udzapita kwa munthu aliyense kumene ndidzakutuma ndi kunena
chilichonse chimene ndidzakulamulira. 8 Usawaope, pakuti Ine ndili
nawe, ndipo ndidzakupulumutsa," akutero Yehova.

9 Pamenepo Yehova anatambalitsa dzanja lake nakhudza pakamwa panga, nandiwuza kuti, "Taona, tsopano ndayika mawu anga m'kamwa
mwako. 10 Lero ndakusankha kuti ukhale ndi ulamuliro pa mitundu
ya anthu ndi pa maufumu awo kuti uzule ndi kugwetsa, uwononge ndi kugumula, kuti uwamange ndi kudzala."

11 Yehova anandifunsa kuti, "Yeremiya, kodi ukuona chiyani?"

Ine ndinayankha kuti, "Ndikuona nthambi ya mtengo wa mtowo."

12 Yehova anandiwuza kuti, "Waona bwino, chifukwa Ine ndikuonetsetsa kuti mawu angawa akwaniritsidwe."

13 Yehova anandifunsanso kachiwiri kuti, "Kodi ukuona chiyani?"

Ine ndinayankha kuti, "Ndikuona m'phika wa madzi owira, ndipo wagudukira kuno kummwera."

14 Yehova anandiwuza kuti, "Mavuto a anthu onse okhala m'dziko lino
adzachokera kumpoto. 15 Ine ndikuyitana anthu onse a ku maufumu a
kumpoto," akutero Yehova.

"Mafumu awo adzabwera ndipo aliyense adzakhazika mpando wake waufumu
polowera pa zipata za Yerusalemu;
iwo adzabwera ndi kuzungulira makoma ake
ndiponso midzi yonse ya dziko la Yuda.

16 Ndidzatulutsa mlandu wanga ndi iwo
chifukwa cha zoyipa zimene anachita pondisiya Ine.
Iwo anakafukiza lubani kwa milungu ina,
ndi kupembedza zimene anapanga ndi manja awo.

17 "Koma iwe Yeremiya konzeka! Nyamuka ndipo ukawawuze zonse zimene ndakulamulira. Usachite nawo mantha, kuopa kuti Ine ndingaku-
chititse mantha iwo akuona. 18 Taona, lero ndakupanga kukhala ngati
mzinda wotetezedwa, ngati mzati wachitsulo ndiponso ngati makoma a

mkuwa kuti usaopsedwe ndi munthu aliyense wa m'dzikomo; kaya ndi
mafumu a Yuda, akuluakulu ake, ansembe ake, kapena munthu wamba
wa m'dzikomo. 19 Iwo adzalimbana nawe koma sadzakugonjetsa, popeza
Ine ndili nawe ndipo ndidzakupulumutsa," akutero Yehova.

# 2

*Aisraeli Asiya Mulungu*

1 Yehova anandiwuza kuti, 2 "Pita ukalengeze kwa anthu a ku
Yerusalemu kuti Yehova akuti,
" 'Ine ndikukumbukira mmene umakhulupirikira pa unyamata wako,
mmene unkandikondera ngati momwe amachitira mkwatibwi,
mmene unkanditsata m'chipululu muja;
m'dziko losadzalamo kanthu.
3 Israeli anali wopatulika wa Yehova,
anali ngati zipatso zake zoyamba kucha pa nthawi yokolola;
onse amene anamuzunza anapezeka kuti ndi olakwa
ndipo mavuto anawagwera,' "
akutero Yehova.

4 Imvani mawu a Yehova, inu zidzukulu za Yakobo,
inu mafuko onse a Israeli.
5 Yehova akuti,
"Kodi makolo anu anandipeza n'cholakwa chanji,
kuti andithawe?
Iwo anatsata milungu yachabechabe,
nawonso n'kusanduka achabechabe.
6 Iwo sanafunse n'komwe kuti, 'Kodi Yehova ali kuti,
amene anatitulutsa m'dziko la Igupto
natitsogolera m'chipululu m'dziko lowuma
ndi lokumbikakumbika,
m'dziko lopanda mvula ndi la mdima,
dziko limene munthu sadutsamo ndipo simukhala munthu aliyense?'
7 Ndinakufikitsani ku dziko lachonde
kuti mudye zipatso zake ndi zabwino zake zina.
Koma inu mutafika munaliyipitsa dziko langa
ndi kusandutsa cholowa changa kukhala chonyansa.
8 Ansembe nawonso sanafunse kuti,
'Yehova ali kuti?'
Iwo amene amaphunzitsa malamulo sanandidziwe;
atsogoleri anandiwukira.
Aneneri ankanenera m'dzina la Baala,
ndi kutsatira mafano achabechabe.

9 "Chifukwa chake Ine ndidzakuyimbaninso mlandu,"
akutero Yehova.
"Ndipo ndidzayimbanso mlandu zidzukulu zanu.
10 Pitani kumadzulo ku chilumba cha Kitimu, ndipo mukaone,
tumizani anthu ku Kedara kuti akafufuze bwino;
ndipo muona kuti zinthu zoterezi sizinachitikepo n'kale lomwe:
11 Kodi ulipo mtundu wa anthu uliwonse umene unasinthapo milungu
yake?
(Ngakhale kuti si milungu n'komwe).
Koma anthu anga asinthitsa Mulungu wawo waulemerero

ndi mafano achabechabe.
12 Inu mayiko akumwamba, dabwani ndi zimenezi,
ndipo njenjemerani ndi mantha aakulu,"
akutero Yehova.
13 "Popeza anthu anga achita machimo awiri:
Andisiya Ine
kasupe wa madzi a moyo,
ndi kukadzikumbira zitsime zawo,
zitsime zong'aluka, zomwe sizingathe kusunga madzi.
14 Israeli si wantchito kapena kapolo wobadwira m'nyumba, ayi.
Nanga n'chifukwa chiyani amuwononga chotere?
15 Adani ake abangulira
ndi kumuopseza ngati mikango.
Dziko lake analisandutsa bwinja;
mizinda yake anayitentha popanda wokhalamo.
16 Ndiponso Aigupto a ku Mefisi ndi a ku Tapanesi
akuphwanyani mitu.
17 Zimenezitu zakuchitikirani
chifukwa munasiya Yehova Mulungu wanu
pamene Iye ankakutsogolerani pa njira yanu?
18 Tsopano mudzapindula chiyani mukapita ku Igupto,
kukamwa madzi a mu Sihori?
Ndipo mudzapindulanji mukapita ku Asiriya,
kukamwa madzi a mu mtsinje wa Yufurate?
19 Kuyipa kwanuko kudzakulangani;
kubwerera m'mbuyo kwanuko kudzakutsutsani.
Tsono ganizirani bwino,
popeza ndi chinthu choyipa
kundisiya Ine Yehova Mulungu wanu;
ndi chinthu chowawa ndithu kusandiopa Ine Mulungu wanu.
Akutero Ambuye Yehova Wamphamvuzonse.

20 "Kuyambira kalekale inu munathyola goli lanu
ndi kudula msinga zanu;
munanena kuti, 'Sitidzakutumikirani!'
Ndithudi, inu mwakhala ngati mkazi wachiwerewere.
Mukupembedza milungu ina pa phiri lililonse lalitali
ndiponso pansi pa mtengo uliwonse wa masamba ambiri.
21 Ine ndinakudzala iwe ngati mtengo wampesa wosankhika;
unali mpesa wabwino kwambiri ndi wodalirika.
Nanga n'chifukwa chiyani wasanduka mpesa
wachabechabe wonga wa kutchire?
22 Ngakhale utasamba ndi soda
kapena kusambira sopo wambiri,
kuthimbirira kwa machimo ako kumaonekabe pamaso panga,"
akutero Ambuye Yehova.
23 "Iwe ukunena bwanji kuti, 'Ine sindinadziyipitse;
sindinatsatire Abaala'?
Takumbukira mmene unkandichimwira m'chigwa muja;
zindikira bwino zomwe wachita.
Iwe uli ngati ngamira yayikazi yaliwiro
yomangothamanga uku ndi uku,
24 wakhala ngati mbidzi yozolowera m'chipululu,

yonka ninunkhiza pa nthawi yachisika.
Ndani angayiretse chilakolako chakecho?
Mphongo iliyonse yoyikhumba sidzavutika.
Pa nthawi yachisika chakecho mphongoyo idzayipeza.
25 Iwe usathamange, nsapato zingakuthere kuphazi
ndi kukhosi kwako kuwuma ndi ludzu.
Koma unati, 'Zamkutu!
Ine ndimakonda milungu yachilendo,
ndipo ndidzayitsatira.'

26 "Monga momwe mbala imachitira manyazi pamene yagwidwa,
moteronso nyumba ya Israeli idzachita manyazi;
Aisraeliwo, mafumu ndi akuluakulu awo,
ansembe ndi aneneri awo.
27 Iwo amawuza mtengo kuti, 'Iwe ndiwe abambo athu,'
ndipo amawuza mwala kuti, 'Iwe ndiye amene unatibala.'
Iwo andifulatira Ine,
ndipo safuna kundiyang'ana;
Koma akakhala pa mavuto amati,
'Bwerani mudzatipulumutse!'
28 Nanga ili kuti milungu yanu imene munadzipangira nokha?
Ibweretu ngati ingathe kukupulumutsani
pamene muli pamavuto!
Inu anthu a ku Yuda,
milungu yanu ndi yambiri kuchuluka kwake ngati mizinda yanu.

29 "Kodi mukundizengeranji mlandu?
Nonse mwandiwukira,"
akutero Yehova.
30 "Ine ndinalanga anthu ako popanda phindu;
iwo sanaphunzirepo kanthu.
Monga mkango wolusa,
lupanga lanu lapha aneneri anu.
31 "Inu anthu a m'bado uno, ganizirani bwino mawu a Yehova:
"Kodi Ine ndinakhalapo ngati chipululu kwa Israeli
kapena ngati dziko la mdima wandiweyani?
Chifukwa chiyani anthu anga akunena kuti, 'Ife tili ndi ufulu omayen-
dayenda;
sitidzabweranso kwa Inu'?
32 Kodi namwali amayiwala zokongoletsera zake,
kapena kuyiwala zovala zake za ukwati?
Komatu anthu anga andiyiwala
masiku osawerengeka.
33 Mumadziwa bwino njira zopezera zibwenzi!
Choncho ngakhale akazi oyipa omwe mumawaphunzitsa njira zanu.
34 Ngakhale pa zovala zako anthu amapezapo
magazi a anthu osauka osalakwa.
Anthuwo simunawapeze akuthyola nyumba.
Komabe ngakhale zinthu zili chomwechi,
35 inu mukunena kuti, 'Ndife osalakwa,
sadzatikwiyira.'
Ndidzakuyimbani mlandu
chifukwa mukunena kuti, 'Ife sitinachimwe.'

36 Chifukwa chiyani
mukunkabe nimusinthasintha njira zanu?
Aigupto adzakukhumudwitsani
monga momwe Asiriya anakuchititsani manyazi.
37 Mudzachokanso kumeneko
manja ali kunkhongo.
Popeza Ine Yehova ndawakana anthu amene munkawadalira,
choncho sadzakuthandizani konse.

# 3

1 "Ngati munthu asudzula mkazi wake
ndipo mkaziyo n'kuchoka nakakwatiwa ndi mwamuna wina,
kodi mwamuna woyambayo angathe kumutenganso mkaziyo?
Kodi atatero sindiye kuti dzikolo layipitsidwa kwambiri?
Koma iwe Israeli wachita zadama ndi zibwenzi zambiri.
Komabe bwerera kwa ine,"
akutero Yehova.
2 "Tayang'ana ku zitunda zowuma.
Kodi aliponso malo ena amene iwe sunachitepo zadama?
Iwe unkakhala m'mbali mwa njira kumadikira zibwenzi zako,
ngati Mluya wobisalira anthu m'chipululu.
Inu mwayipitsa dziko ndi zadama zanu
ndi ntchito zanu zoyipa.
3 N'chifukwa chake Yehova wayimitsa mvula,
ndipo mvula ya nthawi ya masika sinagwe.
Komabe uli ndi maonekedwe a mkazi wachiwerewere;
ndipo sukuchita manyazi ndi pang'ono pomwe.
4 Kodi iwe siposachedwa pomwepa pamene wanena
kuti, 'Abambo anga, Inu bwenzi langa la unyamata wanga,
5 kodi mudzandikwiyira nthawi zonse?
Kodi ukali wanu udzakhalabe mpaka muyaya?'
Umu ndimo mmene umayankhulira,
koma umapitirizabe kuchita zoyipa monga momwe umathera."

### *Kusakhulupirika kwa Israeli*

6 Pa nthawi ya Mfumu Yosiya Yehova anandiwuza kuti, "Kodi waona
zomwe Israeli wosakhulupirika uja wachita? Anakwera pa phiri lililonse
lalitali ndi kupita pa tsinde pa mtengo uliwonse wogudira kukapem-
bedza. Choncho anachita za chiwerewere kumeneko. 7 Ndinaganiza
kuti atachita zonsezi, adzabwerera kwa Ine, koma sanabwerere, ndipo
mlongo wake wosakhulupirika uja, Yuda, anaziona zimenezi. 8 Anaona
kuti ndinasudzula Israeli wosakhulupirikayo ndi kumupirikitsa chifukwa
cha zigololo zake. Komabe Yuda m'bale wake wosakhulupirika uja
sanaope, nayenso anapita kukachita chigololo. 9 Chiwerewere cha Israeli
chinali chochititsa manyazi kotero kuti chinayipitsa dziko lonse. Anachita
chigololo popembedza mafano a miyala ndi mitengo. 10 Israeli atachita
zonsezi, Yuda m'bale wake wosakhulupirika uja sanabwerere kwa Ine ndi
mtima wake wonse, koma mwachiphamaso chabe," akutero Yehova.
11 Yehova anandiwuza kuti, "Kusakhulupirika kwa Israeli n'kochepa
kuyerekeza ndi kusakhulupirika kwa Yuda. 12 Pita ukalalikire kumpoto
uthenga wakuti,
" 'Israeli wosakhulupirikawe, bwerera,' akutero Yehova.

‘Sindidzakukalipira mpaka kalekale,
pakuti ndine wachifundo,’ akutero Yehova.
‘Sindidzakukwiyira mpaka kalekale.
13 Ungovomera kulakwa kwako
kuti unawukira Yehova Mulungu wako.
Vomera kuti unayendayenda kukapembedza milungu yachilendo
pansi pa mtengo uliwonse wogudira,
ndiponso kuti sunandimvere,’ ”
akutero Yehova.

14 “Bwererani, ana osakhulupirika, pakuti ndine mbuye wanu,” akutero
Yehova. “Ndinakusankhani, mmodzimmodzi kuchokera ku mudzi uli-
wonse ndiponso awiriawiri kuchokera ku banja lililonse. 15 Ndipo
ndidzakupatsani abusa a pamtima panga amene adzakutsogolerani
mwanzeru ndi mwaluntha. 16 Masiku amenewo mukadzachulukana
kwambiri m’dzikomo, anthu sadzanenanso za ‘Bokosi la Chipangano
la Yehova’ kapena kuliganizira. Sadzalikumbukiranso kapena kulifuna,
ndipo sadzapanganso lina,”
akutero Yehova.

17 Nthawi imeneyo adzatcha Yerusalemu Mpando Waufumu wa Yehova,
ndipo mitundu yonse ya anthu idzasonkhana mu Yerusalemu pamaso
pa Yehova. Sadzawumiriranso kutsata mitima yawo yoyipa. 18 Masiku
amenewo fuko la Yuda lidzaphatikizana ndi fuko la Israeli, onse pamodzi
adzachokera ku dziko la kumpoto kupita ku dziko limene ndinapatsa
makolo awo, kuti likhale cholowa.

19 “Ine mwini ndinati,
“ ‘Ndikanakonda bwanji kukukhazikani pakati pa ana anga
ndikukupatsani dziko labwino kwambiri,
cholowa chokongola kwambiri kuposa cha mitundu ina ya anthu.’
Ndinaganiza kuti mudzanditcha Ine ‘Atate’
ndi kuti simudzaleka kunditsata.
20 Koma monga mkazi wosakhulupirika amasiya mwamuna wake,
momwemonso inu mwakhala osakhulupirika kwa Ine, inu fuko la Israeli,”
akutero Yehova.

21 Mawu akumveka pa magomo,
Aisraeli akulira ndi kupempha chifundo
chifukwa anatsata njira zoyipa
ndi kuyiwala Yehova Mulungu wawo.

22 Inu mukuti, “Bwererani, anthu osakhulupirika;
ndidzachiritsa kubwerera m’mbuyo kwanu.”

“Inde, tidzabwerera kwa Inu
pakuti ndinu Yehova Mulungu wathu.
23 Ndithu kupembedza pa magomo
komanso kuchita maphwando pa mapiri zilibe phindu.
Zoonadi chipulumutso cha Israeli
chili mwa Yehova Mulungu wathu basi.
24 Kuyambira pa ubwana wathu milungu yochititsa manyazi ija yakhala ikutiwonongetsa phindu
la ntchito za makolo athu,
nkhosa ndi ng’ombe zawo,

ana awo aamuna ndi aakazi.
25 Tilekeni tigone pansi mwa manyazi,
ndipo kunyozeka kwathu kutiphimbe.
Paja tachimwira Yehova Mulungu wathu,
ife pamodzi ndi makolo athu
kuyambira nthawi ya ubwana wathu mpaka lero lino
sitinamvere Yehova Mulungu wathu."

# 4

1 "Ngati mukufuna kubwerera, inu Aisraeli,
bwererani kwa Ine,"
akutero Yehova.
"Chotsani mafano anu onyansa pamaso panga
ndipo musasocherenso.
2 Muzilumbira mokhulupirika ndiponso mwa chilungamo
kuti, 'Pali Yehova wamoyo.'
Mukatero anthu a mitundu ina yonse adzandipempha kuti ndiwadalitse
ndipo adzanditamanda."
3 Zimene Yehova akunena kwa anthu a ku Yuda ndi a ku Yerusalemu
ndi izi:
"Limani masala anu
musadzale pakati pa minga.
4 Dziperekeni nokha kwa Ine
kuti munditumikire ndi mtima wanu wonse,
inu anthu a ku Yuda ndi ku Yerusalemu.
Muzichita zimenezi kuopa kuti mkwiyo wanga ungabuke ngati moto ndi
kukutenthani,
chifukwa cha ntchito zanu zoyipazo
popanda wina wowuzimitsa.

### *Adani Ochokera Kumpoto kwa Yuda*

5 "Lengeza ku Yuda ndi kulalikira mu Yerusalemu kuti,
'Lizani lipenga m'dziko lonse!'
Ndipo fuwulani kuti,
'Sonkhanani!
Tiyeni tithawire ku mizinda yotetezedwa!'
6 Kwezani mbendera kuyang'ana ku Ziyoni!
Musachedwe, thawani kuti mupulumuke!
Pakuti Ine ndikubweretsa chilango kuchokera kumpoto,
kudzakhala chiwonongeko choopsa."

7 Monga mkango umatulukira m'ngaka yake
momwemonso wowononga mayiko
wanyamuka ndi kutuluka ku mbuto yake.
Watero kuti awononge dziko lanu.
Mizinda yanu idzakhala mabwinja
popanda wokhalamo.
8 Choncho valani ziguduli,
lirani ndi kubuwula,
pakuti mkwiyo waukulu wa Yehova
sunatichokere.

9 "Pa tsiku limenelo, mfumu ndi nduna zake adzataya mtima,
ansembe adzachita mantha kwambiri,

ndipo aneneri adzathedwa nzeru,"
akutero Yehova.
10 Ndipo ine ndinati, "Haa, Ambuye Yehova, ndithu munawanyenga
anthu awa pamodzi ndi Yerusalemu pamene munanena kuti, 'Mudzakhala
pa mtendere,' chonsecho lupanga lili pakhosi pathu."
11 Nthawi imeneyo anthu awa ndi Yerusalemu adzawawuza kuti,
"Mphepo yotentha yochokera ku magomo a m'chipululu ikuwomba pa
anthu anga, osati mphepo yopeta kapena yoyeretsa; 12 koma mphepo
yamphamvu kwambiri yochokera kwa Ine. Tsono ndi Ineyo amene
ndikuwaweruza."

13 Taonani, adani akubwera ngati mitambo,
magaleta awo akubwera ngati kamvuluvulu,
akavalo awo ndi aliwiro kupambana chiwombankhanga.
Tsoka ilo! Tawonongeka!
14 Iwe Yerusalemu, tsuka mtima wako kuchotsa zoyipa kuti upulumuke.
Kodi maganizo ako oyipawo udzakhala nawo mpaka liti?
15 Pakuti amithenga akulalika mawu m'dziko la Dani;
akulengeza za masautso kuchokera ku mapiri a Efereimu.
16 Iwo akuti, "Fotokozani zimenezi kwa anthu a mitundu ina,
lengezani zimenezi mu Yerusalemu kuti,
'Ankhondo akubwera kuchokera ku dziko lakutali,
akufuwula ndi kudzazinga mizinda ya Yuda.
17 Azinga Yerusalemu ngati anthu olondera munda,
chifukwa Yerusalemu wandiwukira,' "
akutero Yehova.
18 "Makhalidwe anu ndi zochita zanu
zakubweretserani zimenezi.
Chimenechi ndiye chilango chanu.
N'chowawa kwambiri!
N'cholasa mpaka mu mtima!"

19 Mayo, mayo,
ndikumva kupweteka!
Aa, mtima wanga ukupweteka,
ukugunda kuti thi, thi, thi.
Sindingathe kukhala chete.
Pakuti ndamva kulira kwa lipenga;
ndamva mfuwu wankhondo.
20 Tsoka limatsata tsoka linzake;
dziko lonse lasanduka bwinja.
Mwadzidzidzi matenti athu awonongedwa,
mwa kanthawi kochepa nsalu zake zotchinga zagwetsedwa.
21 Kodi ndikhale ndikuona mbendera ya nkhondo,
ndi kumva kulira kwa lipenga mpaka liti?

22 Yehova akuti, "Anthu anga ndi zitsiru;
iwo sandidziwa.
Iwo ndi ana opanda nzeru;
samvetsa chilichonse.
Ali ndi luso lochita zoyipa,
koma sadziwa kuchita zabwino."

23 Ndinayang'ana dziko lapansi,

ndipo linali lopanda anthu ndi lopanda kanthu;
ndinayang'ana thambo,
koma linalibe kuwala kulikonse.
24 Ndinayang'ana mapiri,
ndipo ankagwedezeka;
magomo onse ankangosunthira uku ndi uku.
25 Ndinayang'ana, ndipo sindinaone anthu;
mbalame iliyonse ya mlengalenga inali itathawa.
26 Ndinayang'ana, dziko lachonde linali litasanduka chipululu;
mizinda yake yonse inali itasanduka bwinja
pamaso pa Yehova, chifukwa cha mkwiyo wake.
27 Yehova akuti,
"Dziko lonse lidzasanduka chipululu
komabe sindidzaliwononga kotheratu.
28 Chifukwa chake dziko lapansi lidzalira
ndipo thambo lidzachita mdima,
pakuti ndayankhula ndipo sindidzafewa mtima,
ndatsimikiza ndipo sindidzabwerera m'mbuyo."

29 Pakumva phokoso la okwera pa akavalo ndi la anthu oponya mivi,
anthu a m'mizinda adzathawa.
Ena adzabisala ku nkhalango;
ena adzakwera m'matanthwe
mizinda yonse n'kuyisiya;
popanda munthu wokhalamo.

30 Iwe Yerusalemu, ndiwe bwinja!
Ukutanthauza chiyani kuvala zovala zofiira
ndi kuvalanso zokometsera zagolide?
Ngakhale udzikonze maso ako powapaka zokometsera,
ukungodzivuta chabe.
Zibwenzi zako zikukunyoza;
zikufuna kuchotsa moyo wako.

31 Ndikumva kulira ngati kwa mayi pa nthawi yake yobereka,
kubuwula ngati kwa mayi amene akubereka mwana wake woyamba.
Kuliraku ndi kwa anthu a mu Ziyoni, wefuwefu.
Atambalitsa manja awo n'kumati,
"Kalanga ife! Tikukomoka.
Moyo wathu waperekedwa kwa anthu otipha."

# 5

*Palibe Munthu Wolungama*

1 "Pitani uku ndi uku m'misewu ya Yerusalemu,
mudzionere nokha,
funafunani m'mabwalo ake.
Ngati mungapeze munthu mmodzi
amene amachita zachilungamo ndi kufunafuna choonadi,
ndipo ndidzakhululukira mzinda uno.
2 Ngakhale anthu akulumbira kuti, 'Pali Yehova wamoyo,'
komabe akungolumbira mwachinyengo."

3 Inu Yehova, kodi suja mumafuna anthu onena zoona?
Inu munawakantha anthuwo, koma sanamve kupweteka;
munawaphwanya anthuwo, koma sanatengepo phunziro.
Anawumitsa mitima yawo ngati mwala
ndipo anakaniratu kulapa.
4 Ndiye ndinati, “Awa ndi amphawi chabe;
anthu ochita zopusa.
Sadziwa njira ya Yehova,
sazindikira zimene Mulungu wawo amafuna.
5 Tsono ndidzapita kwa atsogoleri
ndi kukayankhula nawo;
ndithu iwo amadziwa njira ya Yehova,
amadziwa zomwe Mulungu wawo amafuna.”
Koma ayi, iwonso anathyola goli la Yehova
ndipo anadula msinga zawo.
6 Choncho mkango wochokera ku nkhalango udzawapha,
mmbulu wochokera ku thengo udzawawononga,
kambuku adzawabisalira pafupi ndi mizinda yawo
kuti akhadzule aliyense amene adzayesera kutuluka m'mizindamo
pakuti kuwukira kwawo ndi kwakukulu
ndipo abwerera m'mbuyo kwambiri.

7 Yehova akuti, “Kodi ndingakukhululukireni bwanji ndi zimene mwachita?
Ana anu andisiya Ine
ndipo amapembedza milungu imene si milungu konse.
Ine ndinawapatsa zonse zimene ankasowa,
komabe iwo anachita chigololo
namasonkhana ku nyumba za akazi achiwerewere.
8 Monga amachitira akavalo onenepa akamamemesa,
aliyense wa iwo ankathamangira mkazi wa mnzake.
9 Tsono ndingaleke kuwalanga chifukwa cha zimenezi?”
akutero Yehova.
“Kodi n'kuleka kuwulipsira
mtundu woterewu?

10 “Pitani ku minda yake ya mipesa ndi kukayiwononga,
koma musakayiwononge kotheratu.
Sadzani nthambi zake
pakuti anthu amenewa si a Yehova.
11 Nyumba ya Israeli ndi nyumba ya Yuda
onse akhala osakhulupirika kotheratu kwa Ine.”

12 Iwowa ankanama ponena za Yehova kuti,
“Yehova sangachite zimenezi!
Choyipa sichidzatigwera;
sitidzaona nkhondo kapena njala.
13 Mawu a aneneri azidzangopita ngati mphepo;
ndipo mwa iwo mulibe uthenga wa Yehova.
Choncho zimene amanena zidzawachitikira okha.”
14 Chifukwa chake Yehova Mulungu Wamphamvuzonse akuti,
“Popeza kuti anthu awa ayankhula mawu amenewa,
tsono mawu anga ndidzawasandutsa moto m'kamwa mwako

ndipo anthu awa ndidzawasandutsa nkhuni zimene moto udzapserezeretu.
15 Inu Aisraeli," Yehova akuti,
"Ndikukubweretserani mtundu wa anthu ochokera kutali,
ndi mtundu umene sunagonjetsedwepo,
mtundu wakalekale umene chiyankhulo chawo inu simuchidziwa,
zimene akunena inu simungazimvetse.
16 Zida zawo za nkhondo zapha anthu ambirimbiri;
onsewo ndi ankhondo amphamvu okhaokha.
17 Adzakudyerani zokolola zanu ndi chakudya chanu,
adzapha ana anu aamuna ndi aakazi;
adzakupherani nkhosa zanu ndi ng'ombe zanu,
adzawononga mpesa wanu ndi mikuyu yanu.
Ndi malupanga awo adzagwetsa
mizinda yanu yotetezedwa imene mumayidalira.
18 "Komabe pa masiku amenewo sindidzakuwonongani kotheratu,"
akutero Yehova. 19 Ndipo pamene anthu adzafunsa Yehova kuti,
"Chifukwa chiyani Yehova Mulungu wathu wachita zimenezi?" Iwe
udzawawuze kuti, "Monga momwe mwasiyira Ine ndi kutumikira milungu
yachilendo m'dziko mwanu, momwemonso mudzatumikira anthu a
m'dzikonso lachilendo."
20 "Lengeza izi kwa ana a Yakobo
ndipo mulalikire kwa anthu a ku Yuda kuti,
21 Imvani izi, inu anthu opusa ndi opanda nzeru,
inu amene maso muli nawo koma simupenya,
amene makutu muli nawo koma simumva.
22 Kodi simuyenera kuchita nane mantha?"
Akutero Yehova.
"Kodi simuyenera kunjenjemera pamaso panga?
Ine ndinayika mchenga kuti ukhale malire a nyanja,
malire a muyaya amene nyanjayo singadutsepo.
Mafunde angawombe motani, koma sangathe kupitirira malirewo;
mafunde angakokome motani, koma sangadutse malirewo.
23 Koma anthu awa ndi nkhutukumve ndiponso a mitima yowukira;
andifulatira ndipo andisiyiratu.
24 Sananenepo m'mitima mwawo kuti,
'Tiyeni tizipembedza Yehova Mulungu wathu.
Kodi suja amatipatsa pa nthawi yake mvula yachizimalupsa ndi yamasika.
Iye salephera konse kutipatsa nyengo ya khololola.'
25 Koma zolakwa zanu zalepheretsa zonsezi;
ndipo machimo anu akumanitsani zabwino.

26 "Pakati pa anthu anga pali anthu ena oyipa
amene amabisalira anzawo monga amachitira mlenje mbalame
ndiponso ngati amene amatchera misampha kuti akole anthu anzawo.
27 Nyumba zawo zadzaza ndi chuma chochipeza mwa chinyengo
ngati zikwere zodzaza ndi mbalame.
N'chifukwa chake asanduka otchuka ndi olemera.
28 Ndipo ananenepa ndi kukhala ndi matupi osalala.
Ntchito zawo zoyipa n'zopanda malire;
saweruza mwachilungamo nkhani ya ana amasiye kuti iyende bwino,
sateteza ufulu wa anthu osauka.
29 Kodi Ine ndingaleke kuwalanga chifukwa cha zimenezi?

Kodi ndisawulipsire
mtundu woterewu?
Akutero Yehova.

30 “Chinthu chothetsa nzeru ndi choopsa kwambiri
chachitika m’dzikomo:
31 Aneneri akunenera zabodza,
ndipo ansembe akuvomerezana nawo,
ndipo anthu anga akukonda zimenezi.
Koma mudzatani potsiriza?

# 6

*Kuzingidwa kwa Yerusalemu*

1 “Thawani, inu anthu a ku Benjamini!
Tulukani mu Yerusalemu!
Lizani lipenga ku Tekowa!
Kwezani mbendera ku Beti-Hakeremu!
Pakuti tsoka lalikulu likubwera kuchokera kumpoto,
ndipo chiwonongekocho n’chachikulu.
2 Kodi mzinda wa Ziyoni suli ngati msipu wokongola kwambiri,
kumene abusa amafikako ndi ziweto zawo?
3 Abusa ndi nkhosa zawo adzabwera kudzalimbana nawo;
adzamanga matenti awo mowuzinga,
ndipo aliyense adzakhazika anthu ake pamalo pake.”

4 Adzanena kuti, “Konzekani kuwuthira nkhondo mzindawo!
Nyamukani, kuti tiwuthire nkhondo mzindawu masana ano.
Koma tili ndi tsoka, dzuwa lapendeka,
ndipo zithunzithunzi za kumadzulo zikunka zitalika.
5 Tsono nyamukani kuti tiwuthire nkhondo mzindawu usiku uno
ndi kuwononga malinga ake!”
6 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
“Dulani mitengo
ndipo mumange mitumbira yankhondo kulimbana ndi Yerusalemu.
Mzinda umenewu uyenera kulangidwa;
wadzaza ndi kuponderezana.
7 Monga momwe chitsime chimatulutsira madzi
ndi mmenenso Yerusalemu amatulutsira zoyipa zake.
Chiwawa ndi chiwonongeko ndi zomwe zimamveka mu mzindamo;
nthenda yake ndi mabala ake ndimaziona nthawi zonse.
8 Iwe Yerusalemu, tengapo phunziro,
kuopa kuti chikondi changa pa iwe chingakuchokere
ndi kusandutsa dziko lako kukhala bwinja
mopanda munthu wokhalamo.”
9 Yehova Wamphamvuzonse anandiwuza kuti,
“Adani adzawakunkha ndithu anthu otsala a Israeli,
monga momwe amachitira populula mphesa.
Tsono iwe yesetsa kupulumutsa amene ungathe
monga mmene amachitira munthu wokolola mphesa.”

10 Kodi ndiyankhule ndi yani ndi kumuchenjeza?
Ndinene mawu ochenjeza kwa yani kuti amve?

Makutu awo ndi otsekeka
kotero kuti sangathe kumva.
Mawu a Yehova ndi onyansa kwa iwo;
sasangalatsidwa nawo.
11 Koma ine ndadzazidwa ndi mkwiyo wa Yehova,
ndipo ndatopa ndi kusunga mkwiyo wa Yehova.

Yehova anandiwuza kuti, “Tsono ndidzawutulutsira mkwiyo umenewu pa ana oyenda m’misewu
ndi pa achinyamata amene asonkhana pamodzi;
pakutinso mwamuna ndi mkazi wake adzatengedwa,
pamodzi ndi okalamba amene ali ndi zaka zochuluka.
12 Nyumba zawo adzazipereka kwa ena,
pamodzi ndi minda yawo ndi akazi awo.
Ndidzatambasula dzanja langa kukantha
anthu okhala m’dzikomo,”
akutero Yehova.
13 “Kuyambira wamng’ono mpaka wamkulu,
onse ali ndi dyera lofuna kupeza phindu mwa kuba;
aneneri pamodzi ndi ansembe omwe,
onse amachita zachinyengo.
14 Amapoletsa zilonda za anthu anga
pamwamba pokha.
Iwo amanena kuti, ‘Mtendere, mtendere,’
pamene palibe mtendere.
15 Kodi amachita manyazi akamachita zonyansazo?
Ayi, sachita manyazi ndi pang’ono pomwe;
sadziwa ndi kugwetsa nkhope komwe.
Choncho iwo adzagwera pakati pa anzawo amene agwa kale;
adzagwa pansi tsiku limene ndidzawalange,”
akutero Yehova.
16 Yehova akuti,
“Imani pa mphambano ndipo mupenye;
kumeneko ndiye kuli njira zakale,
funsani kumene kuli njira yabwino. Yendani m’menemo,
ndipo mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu.
Koma inu munati, ‘Ife sitidzayenda njira imeneyo.’
17 Ine ndinakupatsani alonda oti akuyang’anireni
ndipo ndinati, ‘Imvani kulira kwa lipenga!’
koma inu munati, ‘Sitidzamvera.’
18 N’chifukwa chake imvani, inu anthu a mitundu ina;
yang’anitsitsani, inu amene mwasonkhana pano,
chimene chidzawachitikire anthuwo.
19 Imvani, inu anthu okhala pa dziko lapansi,
ndikubweretsa masautso pa anthu awa.
Zimenezi ndi mphotho ya ntchito zawo.
Iwowa sanamvere mawu anga
ndipo anakana lamulo langa.
20 Kodi pali phindu lanji ngakhale mubwere ndi lubani kuchokera ku Seba,
kapena zonunkhira zina kuchokera ku dziko lakutali?
Nsembe zanu zopsereza Ine sindidzalandira;
nsembe zanu sizindikondweretsa.”
21 Choncho Yehova akuti,

“Ndidzayika zokhumudwitsa pamaso pa anthu awa.
Abambo ndi ana awo aamuna onse adzapunthwa ndi kugwa;
anansi awo ndi abwenzi awo adzawonongeka.”
22 Yehova akunena kuti,
“Taonani, gulu lankhondo likubwera
kuchokera kumpoto;
mtundu wa anthu amphamvu wanyamuka
kuchokera kumathero a dziko lapansi.
23 Atenga mauta ndi mikondo;
ndi anthu ankhanza ndi opanda chifundo.
Phokoso lawo lili ngati mkokomo wa nyanja.
Akwera pa akavalo awo
ndipo akonzekera ngati anthu ankhondo,
kudzakuthirani nkhondo anthu a ku Ziyoni.”

24 A ku Ziyoni akuti “Ife tamva mbiri yawo,
ndipo manja anthu alefukiratu.
Nkhawa yatigwira,
ndipo tikumva ululu ngati mayi pa nthawi yake yochira.
25 Musapite ku minda
kapena kuyenda m’misewu,
pakuti mdani ali ndi lupanga,
ndipo ponseponse anthu akuchita mantha.
26 Inu anthu anga, valani ziguduli
ndipo gubudukani pa phulusa;
lirani mwamphamvu
ngati munthu wolirira mwana wake mmodzi yekha,
pakuti mwadzidzidzi wowonongayo
adzabwera kudzatipha.

27 “Iwe Yeremiya, ndakuyika kuti ukhale choyesera zitsulo.
Uwayese anthu anga
monga ungayesere chitsulo
kuti uwone makhalidwe awo.
28 Onsewo ali ndi khalidwe lokanika ndi lowukira
ndipo akunka nanena zamiseche.
Iwo ndi olimba ngati mkuwa ndi chitsulo.
Onse amangochita zoyipa zokhazokha.
29 Moto mu mvukuto ukuyaka kwambiri;
mtovu watha kusungunuka ndi moto.
Koma ntchito yosungunulayo sikupindula
chifukwa zoyipa sizikuchokapo.
30 Iwo ali ngati siliva wotayidwa,
chifukwa Yehova wawakana.”

# 7

*Chipembedzo Chabodza N’chopanda Phindu*

1 Mawu amene Yehova anayankhula kwa Yeremiya ndi awa, 2 “Ima pa
chipata cha Nyumba ya Yehova ndipo kumeneko ukalalikire uthenga uwu:
“ ‘Imvani mawu a Yehova, inu nonse anthu a ku Yuda amene mumalowa
pa chipata ichi kudzapembedza Yehova. 3 Yehova Wamphamvuzonse,
Mulungu wa Israeli akuti: Konzani makhalidwe anu ndi zochita zanu,

ndipo ndidzakulolani kukhala pa malo ano. 4 Musamakhulupirire mawu
anu achinyengo onena kuti, 'Ino ndi Nyumba ya Yehova, Nyumba ya
Yehova, Nyumba ya Yehova!' 5 Ngati mutasinthadi makhalidwe anu ndi
zochita zanu, ndi kumachitirana zolungama, 6 ngati mutaleka kuzunza
mlendo, ana amasiye kapena akazi amasiye ndi kuleka kupha anthu
osalakwa pa malo ano, ndipo ngati muleka kutsatira milungu ina, kuti
ingakuwonongeni, 7 Ine ndidzakulolani kukhala pa malo ano, m'dziko
limene ndinapatsa makolo anu mpaka muyaya. 8 Koma onani, inu
mukudalira mawu abodza amene alibe phindu.

9 "Kodi inu muziba ndi kupha, kuchita chigololo ndi kulumbira
monama, kufukiza lubani kwa Baala ndi kutsatira milungu ina imene
simunayidziwe, 10 ndipo kenaka n'kubwera kudzayima pamaso panga
m'Nyumba ino, Nyumba imene imadziwika ndi Dzina langa, inu n'kumati,
'Tapulumuka.' Mwapulumuka kuti muzichitabe zonyansazi? 11 Kodi
Nyumba ino imene imadziwika ndi Dzina langa, yasanduka phanga la
anthu olanda zinthu anzawo mwachifwamba inu mukuona? Komatu
ndakhala ndi kuziona zonsezi! akutero Yehova."

12 " 'Pitani tsopano ku malo anga ku Silo, malo amene poyamba ankadzi-
wika ndi Dzina langa, ndipo mukaone zimene ndinachita kumeneko chi-
fukwa cha kuyipa kwa anthu anga Aisraeli. 13 Tsono popeza munkachita
zonsezi, ngakhale Ine kukuyankhulani koma inu osamvera, kukuyitanani
koma inu osayankha, 14 choncho ndidzachita pa Nyumba imene imadzi-
wika ndi Dzina langayi, Nyumba ya Yehova imene mumayidalira, malo
amene ndinapereka kwa inu ndi makolo anu, zomwe ndinachita ku
Silo. 15 Ndidzakuthamangitsani pamaso panga, ngati momwe ndinachitira
abale anu onse, anthu a Efereimu.' "

16 "Choncho iwe Yeremiya usawapempherere anthu awa ngakhale
kuwapepesera kapenanso kuwapembedzera; usandidandaulire, chifukwa
Ine sindidzakumvera. 17 Kodi sukuona zimene akuchita m'mizinda ya
ku Yuda ndi m'misewu ya ku Yerusalemu? 18 Ana akutorera nkhuni,
abambo akusonkha moto, ndipo amayi akukanda ufa kuti aphike makeke
oti akapereke nsembe kwa mfumukazi yazakumwamba. Iwo amathira
nsembe ya zakumwa kwa milungu ina kuti andipsetse mtima. 19 Koma
kodi akuvutitsa Ine? Kodi sakungodzivuta okha, ndi kudzichititsa
manyazi? akutero Yehova."

20 "N'chifukwa chake Ambuye Yehova akuti: Ndidzatsanulira mkwiyo
wanga pa Nyumba yangayi, anthu, nyama, mitengo ndi zipatso zomwe.
Mkwiyowo udzakhala ngati moto wosazimitsika.

21 "Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti: Wonjezerani
nsembe zanu zopsereza pa nsembe zanu zinazo ndipo mudye nyama
yakeyo! 22 Pakuti pamene ndinatulutsa makolo anu ku Igupto ndi
kuyankhula nawo, sindinawalamulire kuti azipereka nsembe zopsereza
kapena nsembe zinazo, 23 koma ndinawalamula kuti: Mverani Ine, ndipo
ndidzakhala Mulungu wanu ndipo inu mudzakhala anthu anga. Muzitsata
zonse zimene ndakulamulirani, ndipo zinthu zidzakuyenderani bwino.
24 Koma anthuwo sanamvere kapena kulabadira; m'malo mwake anapi-
tirira kusamvera ndi mitima yawo yoyipa. Iwo anabwerera m'mbuyo
m'malo mopita patsogolo. 25 Kuyambira tsiku limene makolo awo
anachoka ku Igupto mpaka lero lino, ndakhala ndikuwatumizira atumiki
anga, aneneri. 26 Koma anthuwo sanandimvere kapena kusamalira.
Anawumitsa mitima yawo ndi kuchita zoyipa kuposa makolo awo.

27 "Ngakhale iwe uwawuze zonsezi koma sadzakumvera. Ngakhale
uwayitane koma sadzakuyankha. 28 N'chifukwa chake udzawawuze kuti,
'Uwu ndi mtundu wa anthu umene sunamvere Yehova Mulungu wake,
wosalola kulangizidwa. Choonadi chatha; chazimirira pa milomo yawo.'
29 "Tsono meta tsitsi lako ndi kulitaya. Ulire kwambiri pa zitunda
zopanda zomera, pakuti Yehova waukana ndi kuwusiya m'bado umene
wamukwiyitsawu."

### *Chigwa cha Imfa*

30 "Anthu a ku Yuda achita zoyipa pamaso panga, akutero Yehova.
Ayimika mafano awo onyansa m'nyumba imene imadziwika ndi Dzina
langa ndipo ayipitsa. 31 Amanga nsanja yopembedzera Tofeti m'Chigwa
cha Hinomu kuti apserezereko ana awo aamuna ndi aakazi. Zimenezi Ine
sindinawalamulire ngakhale kuziganizira n'komwe. 32 N'chifukwa chake
masiku akubwera, akutero Yehova, pamene anthu sadzawatchulanso mal-
owo Tofeti kapena Chigwa cha Hinomu, koma adzawatchula Chigwa cha
Imfa, chifukwa adzakwirira anthu akufa ku Tofeti mpaka osapezekanso
malo owayika. 33 Ndipo mitembo ya anthu amenewa idzakhala chakudya
cha mbalame zamlengalenga ndi zirombo zakuthengo, ndipo palibe wina
amene adzazipirikitse. 34 Ndidzathetsa nyimbo zonse zachisangalalo ndi
zachikondwerero m'mizinda ya ku Yuda ndi m'misewu ya ku Yerusalemu.
Sikudzamvekanso mawu a chikondwerero a mkwatibwi ndi mkwati
pakuti dzikolo lidzasanduka chipululu."

# 8

1 Yehova akuti, " 'Pa nthawi imeneyo, mafupa a mafumu ndi a
akuluakulu a ku Yuda, mafupa a ansembe ndi a aneneri, ndiponso mafupa
a anthu a ku Yerusalemu adzafukulidwa. 2 Adzawamwaza pa nthaka
kuyang'ana dzuwa, mwezi ndi nyenyezi zonse zamlengalenga, zimene
ankazikonda, kuzitumikira ndi kuzitsatira, kupemphako nzeru ndiponso
kuzilambira. Mafupawo sadzawasonkhanitsa kapena kuwakwirira, koma
adzakhala ngati ndowe pamwamba pa nthaka. 3 Otsala onse a mtundu
woyipawu adzafuna imfa kopambana moyo kulikonse kumene ndidza-
wapirikitsirako, akutero Yehova Wamphamvuzonse.' "

### *Tchimo ndi Chilango Chake*

4 "Tsono awuze anthuwa, 'Yehova akuti:
" 'Kodi anthu akagwa sangadzukenso?
Munthu akasochera kodi sangathe kubwereranso?
5 Chifukwa chiyani nanga anthu awa akupitirirabe kuchimwa, osabwer-
era?
Chifukwa chiyani Yerusalemu akubwerera m'mbuyo?
Iwo akangamira chinyengo;
akukana kubwerera.
6 Ine ndinatchera khutu kumvetsera
koma iwo sanayankhulepo zoona.
Palibe woyipa amene analapapo zoyipa zake,
n'kumati, 'Ine ndachita chiyani?'
Aliyense akutsatira njira yake
ngati kavalo wothamangira nkhondo.
7 Mbalame yotchedwa kakowa ija imadziwa
nthawi yake mlengalenga.
Koma nkhunda, namzeze ndi chingalu

zimadziwa nthawi yonyamukira ulendo,
koma anthu anga sadziwa
malamulo a Yehova.

8 “ ‘Inu mukunena bwanji kuti,
‘Ndife anzeru ndipo timasunga malamulo a Yehova?’
Koma ndi alembi anu
amene akulemba zabodza.
9 Anthu anzeru achita manyazi;
athedwa nzeru ndipo agwidwa.
Iwo anakana mawu a Yehova.
Nanga tsono nzeru zawo ziwapinduliranji?
10 N’chifukwa chake akazi awo ndidzawapereka kwa amuna ena
ndipo minda yawo ndidzayipereka kwa amene adzawagonjetse.
Kuyambira wamng’ono mpaka wamkulu,
onse ali ndi khalidwe lofuna kupeza chuma mwakuba.
Aneneri pamodzi ndi ansembe omwe,
onse amachita zachinyengo.
11 Iwo amapoletsa zilonda za anthu anga
pamwamba chabe
n’kumati, ‘Mtendere, mtendere,’
pamene palibe mtendere.
12 Kodi amachita manyazi akamachita zonyansazi?
Ayi, alibe manyazi ndi pang’ono pomwe;
iwo sadziwa n’kugwetsa nkhope komwe.
Choncho iwo adzagwera pakati pa anzawo amene agwa kale;
adzagwa pansi tsiku limene ndidzawalanga,
akutero Yehova.

13 “ ‘Ndidzatenga zokolola zawo,
Sipadzakhalanso mphesa pa mpesa
kapena nkhuyu pa mkuyu,
ndipo masamba ake adzawuma.
Zinthu zimene ndinawapatsa
ndidzawachotsera.’ ”

14 Koma amati, “Tikukhala pano chifukwa chiyani?
Tiyeni tonse pamodzi
tithawire ku mizinda yotetezedwa
ndi kukafera kumeneko.
Pakuti Yehova Mulungu wathu watsimikiza kuti tiyenera kufa.
Watipatsa madzi aululu kuti timwe,
chifukwa tamuchimwira.
15 Tinkayembekezera mtendere
koma palibe chabwino chomwe chinachitika,
tinkayembekezera kuchira
koma tinakumana ndi zoopsa zokhazokha.
16 Kulira kwa ng’ombe zazimuna za mdani
kukumveka kuchokera ku Dani;
dziko lonse likunjenjemera
chifukwa cha kulira kwa akavalowo.
Akubwera kudzawononga dziko
ndi zonse zimene zili m’menemo.

Adzawononga mzinda ndi onse okhalamo."

17 Yehova akuti, "Onani, ndikukutumizirani njoka zaululu,
mphiri zimene munthu sangathe kuzilodza,
ndipo zidzakulumani,"

18 Ndadzazidwa ndi chisoni kwambiri,
mtima wanga walefukiratu.
19 Imvani kulira kwa anthu anga
kuchokera ku dziko lakutali:
akuti, "Kodi Yehova sali ku Ziyoni?
Kodi mfumu yake sili kumeneko?"

"Chifukwa chiyani akundiputa ndi mafano awo osema,
ndi milungu yawo yachilendo?"

20 "Nthawi yokolola yapita,
chilimwe chapita,
koma sitinapulumuke."

21 Chifukwa cha mavuto a anthu anga, ine ndikumva kuwawa;
ndikungolira ndipo mantha aakulu andigwira.
22 Kodi ku Giliyadi kulibe mankhwala ochiritsa?
Kodi kumeneko kulibe sing'anga?
Nanga chifukwa chiyani mabala
a anthu anga sanapole?

# 9

1 Aa, ndikanakonda kuti mutu wanga ukanakhala chitsime cha madzi,
ndi maso anga ngati kasupe wa misozi!
Ndikanalira usana ndi usiku
kulirira anthu anga amene aphedwa.
2 Ndani adzandipatsa malo
ogona m'chipululu
kuti ndiwasiye anthu anga
ndi kuwachokera kupita kutali;
pakuti onse ndi achigololo,
ndiponso gulu la anthu onyenga.

3 "Amapinda lilime lawo ngati uta.
M'dzikomo mwadzaza
ndi mabodza okhaokha
osati zoonadi.
Amapitirirabe kuchita zoyipa;
ndipo sandidziwa Ine."
Akutero Yehova.
4 "Aliyense achenjere ndi abwenzi ake;
asadalire ngakhale abale ake.
Aliyense amafuna kumudyera m'bale wake masuku pa mutu.
Choncho aliyense amachitira bwenzi lake ugogodi.
5 Aliyense amamunamiza m'bale wake
ndipo palibe amene amayankhula choonadi.

Anapazoloweza pakamwa pawo kunena zabodza;
amalimbika kuchita machimo.
6 Iwe wakhalira m'chinyengo
ndipo ukukana kundidziwa Ine,"
akutero Yehova.
7 N'chifukwa chake Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Taonani, Ine ndidzawasungunula ngati chitsulo ndi kuwayesa.
Kodi ndingachite nawonso
bwanji chifukwa cha machimo awo?
8 Lilime lawo lili ngati muvi wakuthwa;
limayankhula zachinyengo.
Aliyense ndi pakamwa pake amayankhula mawu achikondi kwa mnansi wake,
koma mu mtima mwake amakonzekera zomuchita chiwembu.
9 Kodi ndilekerenji kuwalanga chifukwa cha zimenezi?
akutero Yehova.
'Kodi ndisawulipsire
mtundu wotere wa anthu?' "

10 Ndidzakhetsa misozi ndi kulira kwamphamvu chifukwa cha mapiri
ndipo ndidzadandaula chifukwa cha msipu wa ku chipululu.
Malo onsewo awonongeka ndipo palibe amene amapitako,
ndipo sikumveka kulira kwa ng'ombe.
Mbalame zamlengalenga zathawa
ndipo nyama zakuthengo zachokako.

11 Ndipo Yehova anati, "Ndidzasandutsa Yerusalemu kukhala bwinja,
malo okhalamo ankhandwe;
ndipo ndidzawononga mizinda ya Yuda
kotero kuti palibe munthu amene adzakhalemo."
12 Ine ndinati, "Kodi munthu wanzeru ndani woti n'kumvetsa zimenezi?
Kodi ndani amene Yehova anayankhula naye zimenezi kuti akafotokozere
ena? N'chifukwa chiyani dziko lawonongeka ndi kusanduka chipululu,
m'mene anthu sadutsamo?"
13 Yehova anati, "N'chifukwa chakuti anthuwa analeka kutsata mala-
mulo anga amene ndinawapatsa; sanandimvere kapena kuwasamala.
14 M'malo mwake, anatsatira zolakwa za m'mitima yawo; anapembedza
Abaala ngati momwe makolo awo anawaphunzitsira." 15 Tsono chimene
Ine Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli ndidzachite ndi
anthu amenewa ndi ichi: "Ndidzawadyetsa chakudya cha ziphe ndi
kuwamwetsa madzi a ndulu. 16 Ndidzawabalalitsa pakati pa mitundu ya
anthu imene iwowo kapena makolo awo sanayidziwe, ndipo ndidzawalon-
dola ndi ankhondo mpaka nditawawononga."
17 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Tsopano ganizirani! Muyitane akazi olira mwachisoni kuti abwere;
itanani akazi odziwa kulira bwino."
18 Anthu akuti, "Abwere mofulumira
kuti adzatilire
mpaka m'maso mwathu mutatuluka misozi
ndi kuti msidze zathu zinyowe ndi madzi.
19 Kulira mwachisoni kukumveka kuchokera mu Ziyoni akuti,
'Aa! Ife tawonongeka!
Tachita manyazi kwambiri!

Tiyenera kuchoka m'dziko lathu
chifukwa atipirikitsa m'nyumba zathu.' "

20 Tsono inu amayi, imvani mawu a Yehova;
tcherani makutu anu kuti mumve mawu a Yehova.
Phunzitsani ana anu aakazi kulira mwachisoni;
aliyense aphunzitse mnzake nyimbo ya maliro.
21 Imfa yatifikira kudzera m'mazenera athu
ndipo yalowa m'nyumba zathu zotetezedwa;
yapha ana athu m'misewu,
ndi achinyamata athu m'mabwalo.
22 Yehova anandiwuza kuti ndinene izi kuti,
" 'Mitembo ya anthu
idzakhala ili lambalamba ngati ndowe m'minda,
ngati mapesi m'mbuyo mwa wokolola,
popanda munthu woyitola.' "
23 Yehova akuti,
"Munthu wanzeru asanyadire nzeru zake,
kapena munthu wamphamvu kunyadira nyonga zake,
kapena munthu wolemera kunyadira chuma chake,
24 koma ngati munthu akufuna kunyadira, anyadire chinthu ichi:
kuti iye amamvetsa za Ine ndipo amandidziwa,
kuti ndine Yehova, amene ndimakonda chifundo,
chilungamo ndiponso ungwiro pa dziko lapansi.
Zimenezi ndizo ndimakondwera nazo,"
akutero Yehova.
25 "Nthawi ikubwera," akutero Yehova, "pamene ndidzalanga onse
amene anachita mdulidwe koma mu mtima sasamala n'komwe.
26 Ndidzalanga anthu a ku Igupto, Yuda, Edomu, Amoni, Mowabu,
ndiponso onse amene amakhala kutali ku chipululu. Mitundu ina
yonseyi ndi yosachita mdulidwe, ngakhalenso Aisraeli nawonso sanachite
mdulidwe wa mu mtima."

# 10

*Mulungu ndi Mafano*

1 Inu Aisraeli, imvani zimene Yehova akunena. 2 Yehova akuti,
"Musatsatire makhalidwe a anthu a mitundu ina
kapena kuchita mantha ndi zizindikiro zamlengalenga,
ngakhale anthu a mitundu ina amachita nazo mantha.
3 Pakuti miyambo ya mitundu inayo ndiyachabechabe.
Iwo amakadula mtengo ku nkhalango
ndipo mmisiri amawusema ndi sompho.
4 Amakongoletsa chosemacho ndi siliva ndi golide;
kenaka amachikhomerera ndi misomali
kuti chisagwedezeke.
5 Mafano awo ali ngati mtengo wakanjedza woopsezera mbalame m'munda wa minkhaka.
Mafanowo sangathe n'kuyankhula komwe
ndipo ayenera kunyamulidwa
popeza sangathe n'kuyenda komwe.
Musachite nawo mantha
popeza sangathe kukuchitani choyipa
ndiponso alibe mphamvu yochitira chabwino chilichonse."

6 Palibe wofanana nanu, Inu Yehova;
Inu ndinu wamkulu,
ndipo dzina lanu lili ndi mphamvu yayikulu.
7 Ndani amene angaleke kukuopani,
inu Mfumu ya mitundu ya anthu?
Chimenechi ndicho chokuyenerani.
Pakati pa anthu anzeru onse komanso mafumu onse
a mitundu ya anthu,
palibe wina wofanana nanu.
8 Onsewo ndi opusa ndi opanda nzeru;
malangizo awo amawatenga kuchokera kwa mafano achabechabe opanga ndi mitengo.
9 Siliva wosula amabwera naye kuchokera ku Tarisisi
ndipo golide amachokera naye ku Ufazi.
Mafanowo ndi ntchito ya anthu aluso ndi odziwa kuzokota golide.
Tsono mafanowo amawaveka zovala za mtundu wamtambo ndi pepo.
Yonseyo ndi ntchito ya anthu a luso.
10 Koma Yehova ndiye Mulungu woona;
Iyeyo ndiye Mulungu wamoyo, Mfumu yamuyaya.
Akakwiya, dziko limagwedezeka;
anthu a mitundu ina sangathe kupirira ukali wakewo.
11 "Awuze anthu awa kuti, 'Milungu iyi, imene sinalenge dziko
lakumwamba ndi dziko lapansi, idzawonongeka pa dziko lapansi ndi pansi
pa thambo.' "
12 Koma Mulungu analenga dziko lapansi ndi mphamvu zake;
Iye anapanga dziko lonse ndi nzeru zake
ndipo anayala thambo mwaluso lake.
13 Iye akayankhula, kumamveka mkokomo wamadzi akumwamba;
Iyeyo amabweretsa mitambo kuchokera ku malekezero a dziko lapansi.
Amabweretsa mphenzi pamodzi ndi mvula
ndi kutulutsa mphepo yamkuntho kumalo kumene osungirako.

14 Anthu onse ndi opusa ndiponso opanda nzeru;
mmisiri aliyense wosula golide akuchita manyazi ndi mafano ake.
Mafano akewo ndi abodza;
alibe moyo m'kati mwawo.
15 Mafanowo ndi achabechabe, zinthu zosekedwa nazo.
Pamene anthuwo azidzaweruzidwa, mafanowo adzawonongedwa.
16 Koma Yehova amene ndi Cholowa cha Yakobo sali ngati mafanowo.
Iyeyu ndi Mlengi wa zinthu zonse
kuphatikizapo Israeli, mtundu umene anawusankha kuti ukhale anthu ake.
Dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.

*Chiwonongeko Chikubwera*

17 Sonkhanitsani katundu wanu,
inu amene mukukhala m'linga la ankhondo.
18 Pakuti Yehova akuti,
"Tsopano Ine ndidzachotsa anthu onse
amene akukhala m'dziko lino;
adzakhala pa mavuto

mpaka adzamvetsa.”

19 Aliyense ankangoti, “Mayo ine, chifukwa cha kupweteka kwanga!
Chilonda changa n’chachikulu!”
Koma ine ndinkaganiza kuti, “Ndithu, ili ndi vuto langa basi,
choncho ndingolipirira.”
20 Tenti yanga yawonongeka,
zingwe zake zonse zaduka.
Ana anga andisiya ndipo kulibenso.
Palibenso amene adzandimangire tenti,
kapena kufunyulula nsalu yake.
21 Abusa ndi opusa
ndipo sanapemphe nzeru kwa Yehova;
choncho palibe chimene anapindula
ndipo nkhosa zawo zonse zabalalika.
22 Tamvani! kukubwera mphekesera,
phokoso lalikulu la gulu la a ankhondo likumveka kuchokera kumpoto!
Lidzasandutsa bwinja mizinda ya ku Yuda,
malo okhala nkhandwe.

*Pemphero la Yeremiya*

23 Inu Yehova, ndikudziwa kuti moyo umene munthu ali nawo si wake;
munthuyo sangathe kuwongolera mayendedwe ake.
24 Inu Yehova, langizeni, komatu mwachilungamo,
osati ndi mkwiyo wanu,
mungandiwononge kotheratu.
25 Tsanulirani ukali wanu pa mitundu ya anthu amene sakudziwani,
ndiye kuti mitundu ya anthu amene satama pa dzina lanu mopemba.
Iwo aja anasakaza Yakobo;
amusakaza kotheratu
ndipo awononga dziko lake.

# 11

*Pangano Liphwanyidwa*

1 Yehova anayankhula ndi Yeremiya kuti, 2 “Imvani mawu a pangano
ili, ndipo uwawuze anthu a ku Yuda ndi a ku Yerusalemu. 3 Awuze
kuti Yehova, Mulungu wa Israeli akuti ‘adzakhala wotembereredwa
munthu amene samvera mawu a pangano ili. 4 Awa anali mawu
amene ndinalamulira makolo anu nditawatulutsa mu Igupto, kuchoka
m’ng’anjo yamoto.’ Ine ndinati, ‘Mverani Ine ndi kuchita chilichonse
chimene ndakulamulirani. Mukatero mudzakhala anthu anga ndi Ine
ndidzakhala Mulungu wanu. 5 Tsono Ine ndidzakwaniritsa lumbiro lomwe
ndinalumbira kwa makolo anu kuti ndidzawapatsa dziko loyenda mkaka
ndi uchi,’ dziko lomwe inu lero mukukhalamo.”
Tsono Ine ndinayankha kuti, “Ameni, Yehova.”

6 Yehova anandiwuza kuti, “Lengeza mawu onsewa m’mizinda yonse
ya ku Yuda ndi m’misewu ya mu Yerusalemu: ‘Mverani mawu a pangano
ili ndi kuzitsatira. 7 Kuyambira nthawi imene ndinatulutsa makolo anu
ku Igupto mpaka lero, ndakhala ndi kuwachenjeza kawirikawiri kuti,
‘Mverani Ine.’ 8 Koma sanamvere kapena kulabadirako. Aliyense anawu-
mirira kuchita zoyipa za m’mitima yawo. Ngakhale ndinawalamulira

kuti asunge pangano langa koma iwo sanasunge. Choncho ndinawalanga monga ndinaneneramo.' "
9 Kenaka Yehova anandiwuza kuti, "Anthu a ku Yuda ndi ku Yerusalemu
andiwukira. 10 Abwereranso ku machimo a makolo awo, amene anakana kumvera mawu anga. Akutsata milungu ina ndi kumayitumikira. Aisraeli ndi Ayuda aphwanya pangano limene ndinachita ndi makolo awo.
11 Choncho Yehova akuti, 'Ndidzawagwetsera mavuto amene sadzatha
kuwalewa. Ngakhale adzandilirire, sindidzawamvera. 12 Anthu a
m'mizinda ya Yuda ndi anthu a ku Yerusalemu adzapita ndi kukalirira milungu imene ankayifukizira lubani, koma milunguyo sidzawathandiza
ndi pang'ono pomwe mavuto akadzafika. 13 Iwe Yuda, uli ndi milungu
yochuluka ngati chiwerengero cha mizinda yako; chiwerengero cha maguwa ansembe amene umafukizirapo lubani kwa Baala chili ngati misewu ya mu Yerusalemu.'
14 "Tsono iwe Yeremiya usawapempherere anthu amenewa ngakhale kuwadandaulira kapena kuwapepesera, chifukwa sindidzawamvera akadzandiyitana pa nthawi ya mavuto awo.
15 "Kodi anthu anga okondedwa akudzachita chiyani m'Nyumba yanga?
Kodi suja iwowa amachita zoyipa zambiri?
Kodi mungathe kupulumuka,
tsoka osakugwerani
chifukwa cha nsembe zanuzo?"

16 Kale Yehova ankakutchani mtengo wa olivi wa masamba obiriwira,
wokhala ndi zipatso zokongola.
Koma tsopano adzawutentha
ndi mkuntho wamkokomo
ndipo nthambi zake zidzapserera.
17 Yehova Wamphamvuzonse, amene anakudzalani, walamula kuti
mavuto akugwereni. Inu a banja la Yuda ndi a banja la Israeli munachitira Yehova zoyipa ndi kumukwiyitsa pamene munkapereka nsembe zanu kwa Baala.

*Amuchitira Chiwembu Yeremiya*

18 Yehova anandiwululira ndipo ndinadziwa. Iye anatsekula maso anga
kuti ndione chiwembu chawocho. 19 Ndinali ngati mwana wankhosa
wofatsa amene akupita naye kukamupha; sindinkadziwa kuti chiwembu chimene ankakonzekeracho chinkaloza ine. Iwo amati:
"Tiyeni timuphe
munthu ameneyu
kuti dzina lake lisadzakumbukiridwenso."
20 Koma, Inu Yehova Wamphamvuzonse, Inu amene mumaweruza molungama
ndi kuyesa mitima ndi maganizo,
lolani kuti ine ndione kuti mwawalipsira,
pakuti mlandu wanga ndawupereka m'manja mwanu.
21 "N'chifukwa chake Yehova akunena za anthu a ku Anatoti amene
akufuna kuwononga moyo wako namanena kuti, 'Usanenere m'dzina
la Yehova, ukatero ife tidzakupha ndi manja athu,' 22 koma Yehova
Wamphamvuzonse akuti, 'Ine ndidzawalanga. Achinyamata awo adzaphedwa ndi lupanga, ana awo aamuna ndi aakazi adzafa ndi njala.
23 Sipadzakhala otsala ndi mmodzi yemwe, chifukwa ndidzalanga anthu a
ku Anatoti chikadzafika chaka chawo cha chilango.' "

# 12

### *Madandawulo a Yeremiya*

1 Yehova, Inu mumakhala wokhoza nthawi zonse
ndikati nditsutsane nanu.
Komabe ndikufuna kuyankhula nanu za mlandu wanga.
Chifukwa chiyani anthu oyipa zinthu zimawayendera bwino?
Chifukwa chiyani anthu achinyengo amakhala pabwino?
2 Inu munawadzala ndipo anamera mizu;
amakula ndi kubereka zipatso.
Dzina lanu limakhala pakamwa pawo nthawi zonse,
koma mitima yawo imakhala kutali ndi Inu.
3 Koma Inu Yehova, ine mumandidziwa;
mumandiona ndipo mumayesa zolingalira zanga.
Akokeni anthu oyipawo ngati nkhosa zokaphedwa!
Ayikeni padera mpaka tsiku loti akaphedwe!
4 Kodi dziko lidzakhala likulirabe mpaka liti
ndipo udzu m'munda uliwonse udzakhalabe ofota mpaka liti?
Nyama ndi mbalame kulibiretu
chifukwa anthu amene amakhalamo ndi oyipa.
Iwo amati:
"Yehova sangathe kuona ntchito zathu."

### *Yankho la Mulungu*

5 Yehova anayankha kuti, "Ngati kukutopetsa kuthamanga pamodzi ndi anthu
nanga ungapikisane bwanji ndi akavalo?
Ngati ukupunthwa ndi kugwa pa malo abwino,
udzatha bwanji kuthamanga m'nkhalango
za ku Yorodani?
6 Ngakhale abale ako
ndi anansi akuwukira,
onsewo amvana zokuyimba mlandu.
Usawakhulupirire,
ngakhale ayankhule zabwino ndi iwe.

7 "Ine ndawasiya anthu anga;
anthu amene ndinawasankha ndawataya.
Ndapereka okondedwa anga
m'manja mwa adani awo.
8 Anthu amene ndinawasankha
asanduka ngati mkango wa m'nkhalango.
Akundibangulira mwaukali;
n'chifukwa chake Ine ndikudana nawo.
9 Anthu anga amene ndinawasankha
asanduka ngati mbalame yolusa yamawangamawanga
imene akabawi ayizinga.
Pitani, kasonkhanitseni nyama zakuthengo.
Mubwere nazo kuti zidzadye mbalameyo.
10 Abusa ambiri anawononga munda wanga wa mpesa,
anapondereza munda wanga;
munda wanga wabwino uja
anawusandutsa chipululu.
11 Unawusandutsadi chipululu.

Ukanali wokhawokha chomwecho ukundilirira Ine.
Dziko lonse lasanduka chipululu
chifukwa palibe wolisamalira.
12 Anthu onse owononga abalalikira
ku zitunda zonse za m’chipululu.
Yehova watuma ankhondo ake
kudzawatha kuyambira kumalire ena a dziko mpaka ku malire enanso a dziko,
ndipo palibe amene adzakhale pa mtendere.
13 Anthu anafesa tirigu koma anatuta minga;
anadzitopetsa kugwira ntchito koma osapeza phindu lililonse.
Choncho mudzachita manyazi ndi zokolola zanu
chifukwa cha mkwiyo wa Yehova.”

14 “Anthu oyipa oyandikana ndi anthu anga Aisraeli, akuwalanda
Aisraeliwo dziko, cholowa chimene ndinawapatsa. N’chifukwa chake
ndidzawachotsa m’dziko limenelo, ndipo ndidzachotsa banja la Yuda
pakati pawo. 15 Komabe nditawachotsa, ndidzawachitiranso chifundo,
ndipo ndidzabwezera aliyense cholowa chake ndi dziko lake. 16 Ndipo
ngati iwo adzaphunzira bwino njira za anthu anga ndi kulumbira m’dzina
langa, namanena kuti, ‘Pali Yehova wamoyo,’ monga iwo anaphunzitsira
anthu anga kulumbira m’dzina la Baala, Ine ndidzawakhazikitsa pakati
pa anthu anga. 17 Koma ngati mtundu wina uliwonse sudzamvera, Ine
ndidzawuchotsa ndi kuwuwonongeratu,” akutero Yehova.

# 13

*Lamba Womanga M’chiwuno*

1 Yehova anandiwuza kuti, “Pita kagule lamba wansalu yosalala ndipo
ukavale m’chiwuno mwako, koma usakamuviyike m’madzi.” 2 Choncho
ndinakagula lambayo, monga momwe anandiwuzira Yehova, ndipo ndi-
namanga m’chiwuno mwanga.

3 Kenaka Yehova anandiyankhulanso kachiwiri kuti, 4 “Tenga lamba
amene unagula ndi kuvala m’chiwuno mwako uja. Tsono pita ku mtsinje
wa Yufurate ndipo ukamubise lambayo m’ming’alu ya m’matanthwe.”
5 Ndipo ndinapitadi ndi kukabisa lambayo ku Yufurate, monga anenera
Yehova.

6 Patapita masiku ambiri Yehova anandiwuzanso kuti, “Pitanso ku
Yufurate ndipo ukatenge lamba amene ndinakuwuza kuti ukamubise
kumeneko.” 7 Choncho ndinapita ku Yufurate kukafukula lambayo ndi
kumuchotsa pamalo pamene ndinamubisa, koma nthawi imeneyi n’kuti
lambayo atawonongeka kotheratu ndipo analibenso ntchito.

8 Pamenepo Yehova anandiwuza kuti, 9 “Izi ndi zimene ine ndikunena:
‘Umu ndi mmene ndidzawonongere zimene akunyadira kwambiri a
ku Yuda ndi a ku Yerusalemu. 10 Anthuwa ndi oyipa. Iwo akana
kumvera mawu anga. M’malo mwake amawumirira kutsata milungu ina,
kuyitumikira ndi kuyipembedza. Anthu amenewa adzakhala ngati lamba
wopanda ntchitoyu. 11 Monga momwe lamba amakanirira m’chiwuno
cha munthu, momwemonso ndinakonza kuti nyumba yonse ya Israeli
ndi nyumba yonse ya Yuda indikangamire Ine kuti akhale anthu anga,
kuti azitamanda dzina langa ndi kulemekeza Ine. Koma iwo sanamvere,’
akutero Yehova.

*Zikopa Zothiramo Vinyo*

12 "Awuze anthuwo kuti, 'Yehova Mulungu wa Israeli akuti: Mtsuko
uliwonse adzawudzaza ndi vinyo.' Ndipo ngati iwo anena kwa iwe
kuti, 'Kodi ngati ife sitikudziwa kuti mtsuko uliwonse udzadzazidwa ndi
vinyo?' 13 Tsono iwe uwawuze kuti, Yehova akuti 'Ine ndidzaledzeretsa
anthu onse okhala m'dziko muno, kuyambira mafumu amene amakhala
pa mpando waufumu wa Davide, ansembe, aneneri, pamodzi ndi anthu
onse amene akukhala mu Yerusalemu. 14 Ndidzawagundanitsa mitu
kuti aphwanyane okhaokha ngati mitsuko, makolo ndi ana awo, akutero
Yehova. Sindidzawamvera chisoni kapena kuwachitira chifundo kapena
kukhudzidwa nawo kuti ndileke kuwawononga.' "

### *Yuda Adzapita ku Ukapolo*

15 Imvani inu Aisraeli ndipo tcherani khutu,
musadzitukumule,
pakuti ndi Yehova amene akuyankhula.
16 Lemekezani Yehova Mulungu wanu
asanagwetse mdima,
mapazi anu asanayambe kupunthwa
m'chisisira cham'mapiri.
Asanasandutse kuwala
mukuyembekezerako kukhala
mdima wandiweyani.
17 Koma ngati simumvera,
ndidzalira kwambiri
chifukwa cha kunyada kwanu.
M'maso mwanga
mwadzaza ndi misozi yowawa
chifukwa nkhosa za Yehova zatengedwa ukapolo.

18 Uza mfumu pamodzi ndi amayi ake kuti,
"Tsikani pa mipando yaufumuyo,
pakuti zipewa zanu zaufumu zokongolazo
zagwa pansi."
19 Mizinda ya ku Negevi yatsekedwa
ndipo palibe wina woti n'kuyitsekula.
Yuda yense watengedwa kupita ku ukapolo,
watengedwa yense ukapolo.

20 Tukula maso ako kuti uwone
amene akubwera kuchokera kumpoto.
Kodi nkhosa zimene anakusungitsa zili kuti,
nkhosa zanu zokongola zija?
21 Kodi udzanena chiyani pamene [Yehova] adzakuyikira
anthu amene unkanena kuti ndi abale ako akukugonjetsa ndi kukulamulira?
Kodi sudzamva zowawa
ngati za mayi pa nthawi yake yochira?
22 Ndipo ngati udzadzifunsa kuti,
"Kodi zimenezi zandichitikira chifukwa chiyani?"
Ndi chifukwa cha machimo anu ambiri
kuti zovala zanu zing'ambike
ndiponso kuti akuchitireni nkhanza.

23 Kodi wa dziko la Kusi n'kusintha khungu lake,
kapena kambuku kusintha mawanga ake?
Inunso amene munazolowera kuchita
zoyipa simungathe kusintha.

24 "Ine ndidzakumwazani ngati mankhusu
amene amawuluka ndi mphepo ya ku chipululu.
25 Limeneli ndiye gawo lanu,
chilango chimene ndakukonzerani
chifukwa chondiyiwala Ine
ndi kutumikira milungu yabodza,
akutero Yehova.
26 Ine ndidzakwinya zovala zanu mpaka ku maso
kuti umaliseche wanu uwonekere.
27 Ndaona zonyansa zanu: zigololo zanu, kutchetcherera kwanu
ndi ziwerewere zanu,
zochitika pa mapiri ndi m'minda.
Tsoka iwe Yerusalemu!
Udzakhala wosayeretsedwa
pa zachipembedzo mpaka liti?"

# 14

### *Chilala, Njala, Lupanga*

1 Awa ndi mawu amene Yehova anamuwuza Yeremiya onena za chilala:
2 "Yuda akulira,
mizinda yake ikuvutika;
anthu ake adzigwetsa pansi mwachisoni,
kulira kwa Yerusalemu kwakula.
3 Anthu awo wolemekezeka akutuma antchito awo kuti akatunge madzi.
Apita ku zitsime
osapezako madzi.
Choncho amabwerera ndi mitsuko yopanda madzi.
Amanyazi ndi othedwa nzeru
adziphimba kumaso.
4 Popeza pansi pawumiratu
chifukwa kulibe madzi,
alimi ali ndi manyazi
ndipo amphimba nkhope zawo.
5 Ngakhale mbawala yayikazi
ikusiya mwana wake wakhanda ku thengo
chifukwa kulibe msipu.
6 Mbidzi zikuyima pa zitunda zopanda kanthu
n'kumapuma wefuwefu ngati nkhandwe;
maso awo achita chidima
chifukwa chosowa msipu."

7 Anthu akuti, "Ngakhale machimo athu akutitsutsa,
koma Inu Yehova chitanipo kanthu chifukwa cha dzina lanu.
Pakuti kusakhulupirika kwathu n'kwakukulu;
ife takuchimwirani.
8 Inu Yehova amene Aisraeli amakukhulupirirani
ndi amene mumawapulumutsa pa nthawi ya masautso,

chifukwa chiyani mukukhala ngati mlendo m’dziko muno?
Chifukwa chiyani muli ngati wapaulendo amene akungogona tsiku limodzi?
9 Chifukwa chiyani muli ngati munthu amene wadzidzimutsidwa,
kapena ngati wankhondo amene alibe mphamvu yopulumutsa?
Komabe Inu Yehova, muli pakati pathu,
ndipo tikudziwika ndi dzina lanu;
musatitaye ife!”

10 Zimene Yehova akunena za anthuwa ndi izi:
“Iwo amakonda kuyendayenda kwambiri;
samatha kudziretsa.
N’chifukwa chake Ine Yehova sindingawalandire,
ndipo tsopano ndidzakumbukira zoyipa zawo
ndi kuwalanga chifukwa cha machimo awo.”

11 Kenaka Yehova anandiwuza kuti, “Usawapempherere anthu awa kuti
zinthu ziwayendere bwino. 12 Ngakhale asale zakudya, Ine sindidzamva
kulira kwawo; ngakhale apereke nsembe zopsereza ndi chopereka cha
chakudya, sindidzazilandira. M’malo mwake, ndidzawapha ndi lupanga,
njala ndi mliri.”

13 Koma ine ndinati, “Aa, Ambuye Yehova, aneneri amawawuza
anthuwo kuti, sadzaphedwa ndi lupanga kapena kuvutika ndi njala. Koma
kuti Inu mudzawapatsa mtendere wokhawokha pamalo pano.”

14 Ndipo Yehova anandiwuza kuti, “Ndi zabodza kuti aneneriwa
akunenera m’dzina langa. Ine sindinawatume kapena kuwasankha
kapenanso kuyankhula nawo. Iwo amakuwuzani zinthu zabodza zomwe
amati anaziona m’masomphenya, kapena pogwiritsa ntchito mawula
achabechabe. Zimene amayankhula ndi zongopeka m’mutu mwawo.
15 N’chifukwa chake Ine Yehova ndikuti aneneri amenewa akulosera
m’dzina langa pamene Ine sindinawatume. Iwo amati simudzafa pa
nkhondo kapena ndi njala m’dziko muno. Koma tsono ndi iwowo,
aneneriwa amene adzafe pa nkhondo kapena ndi njala. 16 Ndipo anthu
amene anawaloserawo adzaponyedwa m’misewu ya mu Yerusalemu atafa
ndi njala ndi lupanga. Sipadzapezeka wowayika m’manda popeza iwowo,
akazi awo, ana awo aamuna, onse adzakhala atafa. Ine ndidzawagwetsera
chilango chowayenera.

17 “Awuze mawu awa:
“ ‘Maso anga akugwetsa misozi kosalekeza
usana ndi usiku;
chifukwa anthu anga okondedwa
apwetekeka kwambiri,
akanthidwa kwambiri.
18 Ndikapita kuthengo,
ndikuona amene aphedwa ndi lupanga;
ndikapita mu mzinda,
ndikuona amene asakazidwa ndi njala.
Ngakhale aneneri pamodzi
ndi ansembe onse atengedwa.’ ”

19 Kodi anthu a ku Yuda mwawakana kwathunthu?
Kodi mtima wanu wanyansidwa nawo anthu a ku Ziyoni?
Chifukwa chiyani mwatikantha chotere
kuti sitingathenso kuchira?
Ife tinayembekezera mtendere

koma palibe chabwino chomwe chabwera,
tinayembekezera kuchira
koma panali kuopsezedwa kokhakokha.
20 Inu Yehova, ife tikuvomereza kuyipa kwathu
ndiponso kulakwa kwa makolo athu;
ndithu ife tinakuchimwiranidi.
21 Musatikane kuopa kuti dzina lanu linganyozedwe;
musanyoze mpando wanu waufumu waulemerero.
Kumbukirani pangano lanu ndi ife
ndipo musachiphwanye.
22 Mwa milungu yachabechabe ya anthu a mitundu ina,
kodi pali mulungu amene angagwetse mvula?
Ife chikhulupiriro chathu chili pa Inu,
popeza Inu nokha ndinu Yehova Mulungu wathu
amene mukhoza kuchita zimenezi.

# 15

1 Kenaka Yehova anandiwuza kuti, "Ngakhale Mose ndi Samueli akanay-
ima pamaso panga kupempherera anthu awa, Ine sindikanawachitira
chisoni. Achotseni ndipo ndisawaonenso! Aleke apite! 2 Ndipo ngati
akufunsa iwe kuti, 'Kodi tipite kuti?' uwawuze kuti, 'Yehova akuti,
" 'Oyenera kufa adzafa;
oyenera kufa ndi lupanga adzafa ndi lupanga;
oyenera kufa ndi njala adzafa ndi njala;
oyenera kupita ku ukapolo adzapita ku ukapolo.'
3 "Ine ndidzawatumizira mitundu inayi ya zinthu zowononga," akutero
Yehova, "lupanga lowapha, agalu owaluma, mbalame zamumlengalenga
ndiponso zirombo zoti ziwadye ndi kuwawononga. 4 Ndidzawasandutsa
kukhala chinthu chonyansa kwa anthu a maufumu onse a dziko lapansi
chifukwa cha zimene Manase mwana wa Hezekiya mfumu ya Yuda
anachita mu Yerusalemu.
5 "Kodi adzakumvera chisoni ndani, Yerusalemu?
Kodi adzakulira ndani?
Kodi ndani amene adzapatuka kufunsa za moyo wako?
6 Inu mwandikana Ine," akutero Yehova.
"Inu mukubwererabe m'mbuyo.
Choncho Ine ndidzakukanthani.
Ndatopa ndi kukuchitirani chifundo.
7 Ine ndidzakubalalitsani kukuchotsani m'mizinda ya m'dzikomo
monga mmene amachitira ndi mankhusu popeta ndi lichero.
Anthu anga ndinawaliritsa ndi kuwawononga
chifukwa sanasinthe makhalidwe awo oyipa.
8 Ndinachulukitsa amayi awo amasiye
kupambana mchenga wa kunyanja.
Amayiwo ndinawawonongera ana awo aamuna
dzuwa lili pamutu.
Mwadzidzidzi ndinawagwetsera
kuwawa mtima ndi mantha.
9 Mayi wa ana asanu ndi awiri wakomoka
ndipo akupuma wefuwefu.
Dzuwa lake lalowa ukanali usana;
anamuchititsa manyazi ndipo wathedwa nzeru.

Otsala ndidzawapereka m'manja mwa adani awo
kuti awaphe ndi lupanga,"
akutero Yehova.

10 Kalanga ine, amayi pakuti munandibereka ine,
munthu amene ndikutsutsana ndi kulimbana ndi anthu pa dziko lonse!
Ine sindinakongoze kapena kukongola kanthu,
komatu aliyense akunditemberera.
11 Yehova anati,
"Ndithudi, Ine ndidzakulanditsa kuti upeze bwino.
Ndithudi, adani ako adzakupempha pa nthawi ya tsoka
ndi ya mavuto awo.

12 "Palibe munthu amene angathe kudula chitsulo,
makamaka chitsulo chochokera kumpoto chosakaniza ndi mkuwa.
13 Anthu ako ndi chuma chako
ndidzazipereka kwa ofunkha popanda malipiro,
chifukwa cha machimo anu onse
a m'dziko lanu lonse.
14 Ndidzakusandutsani akapolo a adani anu
m'dziko limene inu simulidziwa,
chifukwa mkwiyo wanga wayaka ngati moto
umene udzakutenthani."

15 Ine ndinati, "Inu Yehova, mumadziwa zonse;
kumbukireni ndi kundisamalira.
Ndilipsireni anthu ondizunza.
Ndilezereni mtima musandilande moyo wanga.
Onani momwe ndi kuvutikira chifukwa cha Inu.
16 Munandiyankhula ndipo mawu anu ndinawalandira bwino.
Mawu anu anandipatsa chimwemwe ndipo mtima wanga unasangalala.
Paja ine, Yehova Mulungu Wamphamvuzonse,
ndimadziwika ndi dzina lanu.
17 Sindinakhale nawo m'gulu la anthu amadyera,
sindinasangalale nawo anthu amenewo.
Ndinakhala ndekha chifukwa choti dzanja lanu linali pa ine
ndipo munadzaza mu mtima mwanga ndi mkwiyo.
18 Nanga n'chifukwa chiyani mavuto anga sakutha?
Bwanji chilonda changa sichikupola?
Kodi inu mudzakhala ngati mtsinje wowuma nthawi yachilimwe,
kapena ngati kasupe wopanda madzi?"
19 Tsono Yehova anandiyankha kuti,
"Ukabwerera kwa Ine, ndidzakulandiranso
ndipo udzakhalanso mtumiki wanga.
Ngati udzayankhula mawu oyenera osati achabechabe,
udzakhalanso mneneri wanga.
Anthu adzabwera kwa iwe
ndipo sipadzafunika kuti iwe upite kwa iwo.
20 Ndidzakusandutsa ngati khoma lolimba
ngati mkuwa kwa anthu awa.
Adzalimbana nawe

koma sadzakugonjetsa,
pakuti Ine ndili nawe
kukulanditsa ndi kukupulumutsa,”
akutero Yehova.
21 “Ndidzakupulumutsa m’dzanja la anthu oyipa
ndipo ndidzakuwombola kwa anthu ankhanza.”

# 16

*Tsiku la Masautso*

1 Kenaka Yehova anandiwuza kuti, 2 “Usadzakwatire ndi kubereka
ana aamuna kapena aakazi malo ano 3 pakuti ana aamuna ndi ana
aakazi obadwira m’dziko muno, komanso amayi awo ndi abambo awo
amene anabereka anawo m’dziko muno, 4 adzafa ndi nthenda zoopsa.
Sadzawalira maliro kapena kuyikidwa m’manda koma adzakhala ngati
ndowe zotayikira pansi. Ena adzaphedwa ku nkhondo ndipo ena
adzafa ndi njala. Mitembo yawo idzakhala chakudya cha mbalame
zamlengalenga ndi zirombo zakuthengo.”
5 Yehova akuti, “Usalowe m’nyumba ya maliro; usapite kukalira
maliro kapena kukapepesa, chifukwa Ine ndawachotsera madalitso anga,
chikondi changa ndi chifundo changa.” 6 Akuluakulu ndi ang’onoang’ono
omwe adzafa m’dziko muno. Sadzayikidwa m’manda kapena kuliridwa,
ndipo palibe amene adzaonetse chisoni podzichekacheka kapena kumeta
tsitsi lake chifukwa cha iwo. 7 Palibe amene adzapereka chakudya kuton-
thoza amene akulira maliro, ngakhale kuti womwalirayo ndi abambo ake
kapena amayi ake.
8 “Ndipo usalowe m’nyumba mmene muli madyerero, n’kukhala pansi
ndi kudya ndi kumwa nawo. 9 Pakuti Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu
wa Israeli akunena kuti, ‘Pa nthawi yanu, inu mukuona ndidzathetsa
mawu achimwemwe ndi achisangalalo ndiponso mawu a mkwati ndi
mkwatibwi pa malo ano.’
10 “Ukawawuza anthu awa zinthu zonsezi akakufunsa kuti, ‘Chifukwa
chiyani Yehova wanena kuti tsoka lalikulu lotere lidzatigwere? Kodi
talakwa chiyani? Kodi tamuchimwira tchimo lotani Yehova Mulungu
wathu?’ 11 Pamenepo ukawawuze kuti, ‘N’chifukwa chakuti makolo
anu anandisiya Ine,’ akutero Yehova, ‘ndi kutsatira milungu ina, kuyitu-
mikira ndi kuyipembedza. Iwo anandisiya Ine ndipo sanasunge lamulo
langa. 12 Komanso inu munachimwa kwambiri kupambana makolo anu.
Aliyense wa inu akutsatira zoyipa ndi mtima wake wokanikawo m’malo
mondimvera Ine. 13 Choncho Ine ndidzakubalalitsani m’dziko muno
ndi kukulowetsani m’dziko limene inu ndi makolo anu simunalidziwe.
Kumeneko mukatumikira milungu ina usana ndi usiku, ndipo sadzaku-
chitirani chifundo.’ ”
14 Yehova akuti, “Komabe masiku akubwera pamene anthu polumbira
sadzatinso, ‘Pali Yehova wamoyo, amene anatulutsa Aisraeli m’dziko la
Igupto,’ 15 koma adzanena kuti, ‘Pali Yehova wamoyo, amene anatulutsa
Aisraeli ku dziko lakumpoto, ndi ku mayiko onse kumene anawabalalitsir-
ako.’ Pakuti ndidzawabwezera ku dziko limene ndinalipereka kwa makolo
awo.”
16 Yehova akuti, “Koma tsopano ndidzayitana adani okhala ngati asodzi
ambiri, ndipo adzawagwira ngati nsomba. Izi zitatha adani enanso
okhala ngati alenje ambiri, adzawasaka pa phiri lililonse, pa chitunda
chilichonse ndiponso m’mapanga onse a m’matanthwe. 17 Maso anga

akuona makhalidwe awo onse; sanabisike pamaso panga. Palibe tchimo
limene sindikulidziwa. 18 Ndidzawalanga mowirikiza chifukwa cha kuyipa
kwawo ndi tchimo lawo. Ndidzatero chifukwa ayipitsa dziko langa ndi
mafano awo amene ali ngati mitembo, ndiponso adzaza cholowa changa
ndi mafano awo onyansa."

19 Inu Yehova, ndinu mphamvu yanga ndi linga langa,
pothawirapo panga nthawi ya masautso,
anthu a mitundu yonse adzabwera kwa Inu
kuchokera ku mathero onse a dziko lapansi ndipo adzanena kuti,
"Makolo anthu anali ndi milungu yonama,
anali ndi mafano achabechabe amene sanawathandize.
20 Kodi anthu n'kudzipangira milungu?
Atati atero ndiye kuti imeneyo ikhala milungu yachabechabe."

21 "Choncho Ine ndidzawaphunzitsa,
kokha kano kuti adziwe
za mphamvu yanga ndi za nyonga zanga.
Pamenepo adzadziwa kuti
dzina langa ndi Yehova.

# 17

1 "Tchimo la Yuda lazokotedwa ndi cholembera cha chitsulo,
lalembedwa ndi msonga ya mwala wadayimondi.
Uchimowo walembedwa pa mitima yawo
ndiponso pa nyanga za maguwa awo.
2 Ngakhale ana awo amakumbukira
maguwa awo ndi zoyimiritsa ngati zifanizo za mulungu wawo Asera,
pa tsinde la mitengo ya masamba ambiri,
pa mapiri aatali m'dzikomo.
3 Chuma chanu ndiponso katundu wanu yense
ndidzazipereka kwa ofunkha
kuti zikhale dipo lawo
chifukwa cha machimo
ochitika m'dziko lonse.
4 Mudzataya dziko limene ndinakupatsani
kuti likhale cholowa chanu.
Ndidzakusandutsani akapolo otumikira adani anu
m'dziko limene inu simukulidziwa,
chifukwa mwabutsa mkwiyo wanga ngati moto,
ndipo udzayaka mpaka muyaya."

5 Yehova akuti,
"Ndi wotembereredwa munthu amene amadalira munthu mnzake,
amene amatsamira pa munthu mnzake kuti amuthandize
pamene mtima wake wafulatira Yehova.
6 Munthuyo adzakhala ngati chitsamba m'chipululu;
iye sadzapeza zabwino.
Adzakhala m'chipululu mopanda madzi,
m'dziko lamchere limene munthu sangathe kukhalamo.

7 "Koma ndi wodala munthu amene amadalira Yehova,
amene amatsamira pa Iye.

8 Adzakhala ngati mtengo wodzalidwa m'mphepete mwa madzi
umene umatambalitsa mizu yake m'mbali mwa mtsinje.
Mtengowo suopa pamene kukutentha;
masamba ake amakhala obiriwira nthawi zonse.
Suchita mantha pa chaka cha chilala
ndipo sulephera kubereka chipatso."

9 Mtima wa munthu ndi wonyenga kupambana zinthu zonse
ndipo kuyipa kwake n'kosachizika.
Ndani angathe kuwumvetsa?

10 "Ine Yehova ndimafufuza mtima
ndi kuyesa maganizo,
ndimachitira munthu aliyense molingana ndi makhalidwe ake
ndiponso moyenera ntchito zake."

11 Munthu amene amapeza chuma mwachinyengo
ali ngati nkhwali imene imafungatira mazira amene sinayikire.
Pamene ali pakatikati pa moyo wake, chumacho chidzamuthera,
ndipo potsiriza adzasanduka chitsiru.

12 Nyumba yathu yopemphereramo ili ngati mpando waufumu waulemerero
wokhazikitsidwa pa phiri lalitali chiyambire.
13 Inu Yehova, chiyembekezo cha Israeli,
onse amene amakusiyani adzachita manyazi.
Iwo amene amakufulatirani mayina awo adzafafanizika ngati olembedwa pa fumbi
chifukwa anakana Yehova,
kasupe wa madzi amoyo.

14 Inu Yehova, chiritseni, ndipo ndidzachira;
pulumutseni ndipo ndidzapulumuka,
chifukwa ndinu amene ndimakutamandani.
15 Anthu akumandinena kuti,
"Mawu a Yehova ali kuti?
Zichitiketu lero kuti tizione!"
16 Ine sindinakuwumirizeni kuti muwalange.
Mukudziwa kuti ine sindilakalaka tsiku la tsoka.
Zonse zimene ndinayankhula Inu mukuzidziwa.
17 Musandichititse mantha;
ndinu pothawira panga pa tsiku la mavuto.
18 Ondizunza anga achite manyazi,
koma musandichititse manyazi;
iwo achite mantha kwambiri,
koma ine mundichotsere manthawo.
Tsiku la mavuto liwafikire;
ndipo muwawononge kotheratu.

### *Kusunga Tsiku la Sabata*

19 Yehova anandiwuza kuti, "Pita ukayime pa chipata chodzerapo anthu,
chimene mafumu a ku Yuda amalowerapo ndi kutulukirapo. Ukayimenso
pa zipata zina zonse za Yerusalemu.
20 Ukawawuze kuti, 'Imvani mawu

a Yehova, inu mafumu onse a ku Yuda ndi anthu onse a ku Yuda
ndi inu nonse okhala mu Yerusalemu amene mumatulukira pa zipata
izi.' [21] Yehova akuti: samalani kuti pa tsiku la Sabata musanyamule
katundu kapena kulowa naye pa zipata za Yerusalemu. [22] Musalowetse
katundu m'nyumba zanu kapena kugwira ntchito pa tsiku la Sabata,
koma mulipatule tsiku la Sabatalo, monga ndinalamulira makolo anu.
[23] Komatu iwo sanandimvere kapena kulabadira. Ndi mitima yawo
yowumayo sanamvere kapena kulandira malangizo anga. [24] Yehova akuti,
'Muzimvera Ine ndi kuleka kulowetsa kapena kutulutsa katundu pa zipata
za mzinda pa tsiku la Sabata. Muzisunga tsiku la Sabata kuti likhale
lopatulika posachita ntchito iliyonse pa tsikuli. [25] Mukatero ndiye mafumu
anu amene akukhala pa mpando wa Davide adzatulukira pa zipata za
mzindawu pamodzi ndi nduna zawo. Iwo pamodzi ndi nduna zawo
azidzalowa atakwera magaleta ndi akavalo, akuperekezedwa ndi anthu
a ku Yuda ndi amene amakhala mu Yerusalemu, ndipo mu mzinda muno
mudzakhala anthu mpaka muyaya. [26] Anthu adzabwera kuchokera ku
mizinda ya Yuda ndi ku midzi yozungulira Yerusalemu, kuchokera ku
dziko la Benjamini ndi ku mapiri a kumadzulo, kuchokera ku dziko la
mapiri ndi ku Negevi. Adzabwera ndi nsembe zopsereza, nsembe zaufa
ndi za chakudya, nsembe za lubani ndi zopereka zachiyamiko ku nyumba
ya Yehova. [27] Koma ngati simundimvera; mukapanda kusunga tsiku la
Sabata kuti likhale lopatulika ndi kumanyamula katundu n'kumalowa
naye pa zipata za Yerusalemu pa tsikuli, Ine ndidzabutsa moto pa zipata
za Yerusalemu. Moto umenewo udzanyeketsa nyumba zaufumu za ku
Yerusalemu ndipo moto wake sudzazima.' "

# 18

### *Ku Nyumba ya Wowumba Mbiya*

[1] Yehova anawuza Yeremiya kuti, [2] "Pita ku nyumba ya munthu
wowumba mbiya, ndipo kumeneko ndikakuwuza mawu anga." [3] Choncho
ndinatsikira ku nyumba ya wowumba mbiya, ndipo ndinamuona
akuwumba mbiya pa mkombero. [4] Tsono amati ngati mbiya imene
waumba ikhala yosawumbika bwino ankayiphwanya n'kuwumbanso ina
monga mmene afunira ndi dothi lake lomwe lija.

[5] Kenaka Yehova anandiwuza kuti, [6] "Inu Aisraeli, kodi Ine sindingathe
kuchita nanu monga amachitira wowumba mbiya?" akutero Yehova.
"Inu muli m'manja mwanga ngati mtapo m'manja mwa wowumba
mbiya. [7] Ngati nditalengeza kuti mtundu wina wa anthu kapena
ufumu wina ndiwuzula, kuwugwetsa ndi kuwuwononga, [8] ndipo ngati
mtundu wa anthu umene ndawuchenjezawo ulapa zoyipa zawo, ndiye
kuti Ine ndidzaleka ndipo sindidzabweretsa pa anthuwo mavuto amene
ndinakonzekera kuwachitira. [9] Ndipo ngati ndilengeza kuti ndikufuna
kumanga ndi kukhazikitsa mtundu wa anthu kapena ufumu. [10] Koma
mtunduwo ukachita choyipa pamaso panga n'kusandimvera, ndiye kuti
sindidzawuchitiranso zabwino zimene ndimafuna ndiwuchitire.

[11] "Ndipo tsopano kawawuze anthu a ku Yuda ndi amene akukhala
mu Yerusalemu kuti, 'Yehova akuti, Taonani! Ndikukukonzerani mavuto,
ndi kuganizira zoti ndikulangeni. Kotero siyani makhalidwe anu oyipa
aliyense wa inu, ndipo mukonzenso makhalidwe anu ndi zochita zanu.'
[12] Koma iwo adzayankha kuti, 'Zimenezo n'zosathandiza. Ife tidzapitiriza

kuchita zomwe takonzekera; aliyense wa ife adzatsatira zoyipa za mtima wake wokanika.' "

13 Yehova akuti,
"Uwafunse anthu a mitundu ina kuti:
Kodi ndani anamvapo zinthu zofanana ndi zimenezi?
Israeli amene anali ngati namwali wanga wachita
chinthu choopsa kwambiri.
14 Kodi chisanu chimatha pa matanthwe
otsetsereka a phiri la Lebanoni?
Kodi madzi ozizira amitsinje ochokera
ku phiri la Lebanoni adzamphwa?
15 Komatu anthu anga andiyiwala;
akufukiza lubani kwa mafano achabechabe.
Amapunthwa m'njira
zawo zakale.
Amayenda m'njira zachidule
ndi kusiya njira zabwino.
16 Dziko lawo amalisandutsa chipululu,
chinthu chochititsa manyazi nthawi zonse;
onse odutsapo adzadabwa kwambiri
ndipo adzapukusa mitu yawo.
17 Ngati mphepo yochokera kummawa,
ndidzawabalalitsa pamaso pa adani awo;
ndidzawafulatira osawathandiza
pa tsiku la mavuto awo."

18 Anthuwo anati, "Tiyeni, tipangane zoti timuchitire Yeremiya; pakuti
ansembe otiphunzitsa malamulo tidzakhala nawobe. Anthu anzeru otilan-
giza tidzakhala nawo, ndiponso aneneri otilalikira mawu. Choncho tiyeni
timupezere chifukwa ndipo tisamvere chilichonse chimene akunena."
19 Ndipo ndinapemphera kwa Yehova kuti, "Inu Yehova, ndimvereni;
imvani zimene adani anga akunena za ine!
20 Kodi chinthu choyipa n'kukhala dipo la chinthu chabwino?
Komabe iwo andikumbira dzenje.
Kumbukirani kuti ndinadzayima pamaso panu
kudzawapempherera
kuti muwachotsere mkwiyo wanu.
21 Choncho langani ana awo ndi njala;
aperekeni kuti aphedwe ndi lupanga.
Akazi awo asanduke opanda ana ndi amasiye;
amuna awo aphedwe ndi mliri,
anyamata awo aphedwe ndi lupanga ku nkhondo.
22 Kulira kumveke kuchokera m'nyumba zawo
mutawatumizira gulu lankhondo mwadzidzidzi kuti liwakanthe.
Iwo andikumbira dzenje kuti ndigweremo
ndipo atchera msampha mapazi anga.
23 Koma Inu Yehova, mukudziwa
ziwembu zawo zonse zofuna kundipha.
Musawakhululukire zolakwa zawo
kapena kufafaniza machimo awo pamaso panu.
Agonjetsedwe pamaso panu;
muwalange muli wokwiya."

# 19

[1] Yehova anandiwuza kuti, “Pita ukagule m’phika wadothi kwa munthu
wowumba. Utenge akuluakulu ena a anthuwa ndi ansembe [2] ndipo mupite
ku Chigwa cha Hinomu chimene chili pafupi ndi pa chipata cha mapale.
Pamenepo ukalengeze mawu amene ndikakuwuze. [3] Ukanene kuti, ‘Im-
vani mawu a Yehova, inu mafumu a ku Yuda ndi anthu a ku Yerusalemu.
Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli, akuti: Tamverani! Ine
ndibweretsa mavuto pa malo pano mwakuti aliyense amene adzamve
adzadzidzimuka. [4] Pakuti anthu andikana Ine ndipo ayipitsa malo
ano. Afukiza lubani pa malo ano kwa milungu imene iwo ngakhale
makolo awo ngakhalenso mafumu a ku Yuda sanayidziwe. Iwo adzaza
malowa ndi magazi a anthu osalakwa. [5] Amanga nsanja zopembedzerapo
Baala, kuperekapo ana awo kuti akhale nsembe zopsereza kwa Baala,
chinthu chimene Ine sindinalamule kapena kuchiyankhula, ngakhalenso
kuchiganizira. [6] N’chifukwa chake taonani, masiku akubwera, akutero
Yehova, pamene anthu sadzatchulanso malo ano kuti Tofeti kapena
Chigwa cha Hinomu, koma Chophera anthu.

[7] “ ‘Pamalo pano ndidzasokoneza maganizo a anthu a ku Yuda ndi
a ku Yerusalemu. Ndidzachititsa kuti adani awo awaphe ku nkhondo.
Ndidzawakanthitsa kwa anthu amene akuwazonda. Mitembo yawo
ndidzayipereka kwa mbalame za mlengalenga ndi zirombo za kutchire
kuti ikhale chakudya chawo. [8] Mzinda uno ndidzawusakaza ndi kuwu-
sandutsa chinthu chochititsa mantha ndi chonyansa. Onse odutsamo
adzadabwa ndi kupukusa mitu yawo chifukwa cha kuwonongeka kwake.
[9] Adani awo adzawuzinga mzindawo kufuna kuwapha motero kuti anthu
a m’katimo adzafika pomadyana wina ndi mnzake. Adzadya ana awo
aamuna ndi ana awo aakazi.’

[10] “Tsono iwe udzaphwanye mtsukowo anthu amene udzapite nawowo
akuona, [11] ndipo ukawawuze kuti, ‘Yehova Wamphamvuzonse akuti, Ine
ndidzaphwanya dziko lino ndi mzinda uno ngati momwe wowumba
amaphwanyira mbiya yake ndipo sangathe kuyikonzanso. Adzayika anthu
akufa ku Tofeti chifukwa padzasowa malo ena owayika. [12] Umu ndi
mmene ndidzachitire ndi malo ano pamodzi ndi anthu okhalamo, akutero
Yehova. Ndidzasandutsa mzindawu kukhala ngati Tofeti. [13] Nyumba za
mu Yerusalemu ndi za mafumu a ku Yuda ndidzazisandutsa ngati za ku
Tofeti chifukwa ndi nyumba zimene pa madenga ake ankafukiza lubani
kwa zolengedwa zamlengalenga ndi kuthira nsembe zachakumwa kwa
milungu ina.’ ”

[14] Kenaka Yeremiya anabwerako ku Tofeti, kumene Yehova anamu-
tuma kuti akanenere, nakayimirira m’bwalo la Nyumba ya Yehova ndi
kuwawuza anthu kuti, [15] “Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli,
akuti, ‘Tamverani! Ine ndidzabweretsa masautso amene ndinanena aja
pa mzinda uno ndi pa mizinda yozungulira, chifukwa anthu ake ndi
nkhutukumve ndipo sanamvere mawu anga.’ ”

# 20

*Yeremiya ndi Pasuri*

[1] Wansembe Pasuri mwana wa Imeri, woyang’anira wamkulu wa
Nyumba ya Yehova, anamva Yeremiya akulosera zinthu zimenezi. [2] Tsono
iye analamula kuti mneneri Yeremiyayo amenyedwe ndi kuyikidwa
m’ndende pa Chipata chakumtunda kwa Benjamini ku Nyumba ya

Yehova. 3 Mmawa mwake, Pasuri anatulutsa Yeremiya m'ndende, ndipo
Yeremiyayo anamuwuza kuti, “Pasuri, Yehova sadzakutchulanso dzina
lako kuti Pasuri koma Zoopsa pa Mbali Zonse. 4 Pakuti Yehova akuti,
‘Ndidzakusandutsa choopsa kwa mwiniwakewe ndi kwa abwenzi ako
onse; iweyo ukuona. Anthu a ku Yuda ndidzawapereka onse m'manja
mwa mfumu ya ku Babuloni. Ena adzatengedwa ukapolo ku Babuloni
ndipo ena adzaphedwa pa nkhondo. 5 Ndidzapereka kwa adani awo
chuma chonse cha mu mzinda uno, phindu lonse la ntchito yake, zinthu
zake zonse za mtengowapatali ndiponso katundu yense wa mafumu a ku
Yuda. Iwo adzazitenga monga zinthu zolanda ku nkhondo ndi kupita
nazo ku Babuloni. 6 Ndipo iwe, Pasuri, pamodzi ndi onse a pa banja
pako mudzapita ku ukapolo ku Babuloni. Mudzafera kumeneko ndi
kuyikidwa m'manda, iweyo pamodzi ndi abwenzi ako amene unawalosera
zabodza.' ”

*Madandawulo a Yeremiya*

7 Inu Yehova, mwandinamiza, ndipo ndinapusadi;
Inu ndi wamphamvu kuposa ine ndipo munandipambana.
Anthu akundinyoza tsiku lonse.
Aliyense akundiseka kosalekeza.
8 Nthawi iliyonse ndikamayankhula,
ndimafuwula kunena kuti, ziwawa kuno! Tikuwonongeka!
Mawu anu Yehova andisandutsa chinthu chonyozeka
ndipo ndimachitidwa chipongwe tsiku lonse.
9 Koma ndikanena kuti, “Sindidzalalikiranso za Iye
kapena kuyankhulanso m'dzina lake,”
mawu anu amayaka ngati moto mu mtima mwanga,
amakhaladi ngati moto wotsekeredwa m'mafupa anga.
Ndapirira kusunga mawu anu mu mtima mwanga osawatulutsa,
koma sindingathe kupirirabe.
10 Ndimamva anthu ambiri akunong'ona kuti,
“Zoopsa ku mbali zonse!
Kamunenezeni! Tiyeni tikamuneneze!”
Onse amene anali abwenzi anga
akuyembekezera kuti ndigwa pansi, akumanena kuti,
“Mwina mwake adzanyengedwa;
tidzamugwira
ndi kulipsira pa iye.”

11 Koma Yehova ali nane, ndiye wankhondo wamphamvu.
N'chifukwa chake ondizunza adzalephera ndipo sadzandipambana.
Adzachita manyazi kwambiri chifukwa sadzapambana.
Manyazi awo sadzayiwalika konse.
12 Inu Yehova Wamphamvuzonse, Inu amene mumayesa anthu molungama
ndipo mupenya za mu mtima mwa munthu.
Ndiloleni kuti ndione kuti mwalipsira adani anga
popeza ndapereka mlandu wanga kwa Inu.

13 Imbirani Yehova!
Mutamandeni Yehova!
Iye amapulumutsa wosauka
m'manja mwa anthu oyipa.

14 Litembereredwe tsiku limene ndinabadwa!
Tsiku limene amayi anga anandibereka lisatamandidwe!
15 Wotembereredwa munthu amene anapita kukasangalatsa abambo anga ndi uthenga woti:
"Kwabadwa mwana wamwamuna!"
16 Munthu ameneyo akhale ngati mizinda imene
Yehova anayiwononga mopanda chisoni.
Amve mfuwu mmawa,
phokoso la nkhondo masana.
17 Chifukwa sanandiphere m'mimba,
kuti amayi anga asanduke manda anga,
mimba yawo ikhale yayikulu mpaka kalekale.
18 Kodi ndinabadwira mavuto ndi chisoni
kuti moyo wanga
ukhale wamanyazi wokhawokha?

# 21

*Mulungu Akana Pempho la Zedekiya*

1 Mfumu Zedekiya inatuma Pasuri mwana wa Malikiya ndi wansembe
Zefaniya mwana wa Maseya kwa Yeremiya. 2 Iwo amati akanene kwa
Yeremiya mawu akuti, "Tinenere kwa Yehova chifukwa Nebukadinezara
mfumu ya Babuloni akutithira nkhondo. Mwina mwake Yehova
n'kutichitira zodabwitsa kuti Nebukadinezarayo achoke kwathu kuno."
3 Koma Yehova anawuza Yeremiya kuti ayankhe Pasuri ndi Zefaniya
kuti, "Kamuwuzeni Zedekiya kuti, 4 'Yehova, Mulungu wa Israeli akuti
ndikulandeni zida zimene zili m'manja mwanu zimene mukugwiritsa
ntchito polimbana ndi mfumu ya ku Babuloni ndi ankhondo ake amene
akuzingani kunja kwa lingali. Ndipo ndidzasonkhanitsa zidazo m'kati
mwa mzindawu. 5 Ineyo mwini wakene ndi mkono wotambasula ndi
dzanja lamphamvu, ndidzachita nanu nkhondo ndili wokwiya, wokalipa
ndi waukali. 6 Ndidzakantha amene amakhala mu mzinda muno, anthu
pamodzi ndi zirombo, ndipo zidzafa ndi mliri woopsa. 7 Pambuyo
pake, ndidzapereka Zedekiya mfumu ya ku Yuda, nduna zake pamodzi
ndi anthu a mu mzinda muno amene adzapulumuke pa nthawi ya
mliri, lupanga ndi njala kwa Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni
ndi kwa adani awo amene ankafuna kuwapha. Iye adzawapha ndi
lupanga. Sadzawachitira chifundo kapena kuwamvera chisoni kapenanso
kuwakomera mtima.'
8 "Yehova anati ndiwawuzenso anthu amenewa kuti asankhe pakati
pa moyo ndi imfa. 9 Aliyense amene akhale mu mzinda muno adza-
phedwa ndi lupanga, njala kapena mliri. Koma aliyense amene apite
kukadzipereka kwa Ababuloni amene akuzinganiwa adzakhala ndi moyo,
adzapulumuka. 10 Ine ndatsimikiza kuchitira mzinda uno choyipa osati
chabwino, akutero Yehova. Udzaperekedwa m'dzanja la mfumu ya ku
Babuloni, ndipo iyeyo adzawutentha ndi moto.
11 "Komanso, uwuze banja laufumu la Yuda kuti, 'Imva mawu a Yehova;
12 inu a m'banja la Davide, Yehova akuti,
" 'Weruzani mwachilungamo mmawa uliwonse;
pulumutsani m'dzanja la wozunza
aliyense amene walandidwa katundu wake,
kuopa kuti ukali wanga ungabuke

ndi kuyaka ngati moto wosazimitsika
chifukwa cha zoyipa zimene mwachita.
13 Ndidzalimbana nanu,
inu amene mukukhala pamwamba pa chigwa,
inu okhala ngati thanthwe lapachidikha,
akutero Yehova.
Inu amene mumanena kuti, ‘Ndani amene angabwere kudzalimbana nafe?
Ndani amene angathe kulowa m’malinga mwathu?’
14 Ndidzakulangani molingana ndi ntchito zanu,
akutero Yehova.
Ndidzatentha nkhalango zanu;
moto udzapsereza zonse zimene zakuzungulirani.’ ”

# 22

*Chiweruzo kwa Mafumu Oyipa*

1 Yehova anandiwuza kuti, “Pita ku nyumba ya mfumu ya ku Yuda ndipo
ukayiwuze kuti, 2 ‘Imva mawu a Yehova, iwe mfumu ya ku Yuda, amene
umakhala pa mpando waufumu wa Davide; iwe, nduna zako pamodzi
ndi anthu ako amene amalowera pa zipata izi. 3 Yehova akuti, uziweruza
molungama ndi mosakondera. Uzipulumutsa munthu amene walandidwa
katundu m’dzanja la womuzunza. Usazunze kapena kupondereza mlendo,
ana amasiye kapena akazi amasiye. Usaphe munthu wosalakwa pa malo
pano. 4 Pakuti ngati udzamvera malamulo awa, ndiye kuti mafumu
onse okhala pa mpando waufumu wa Davide azidzalowabe pa zipata za
nyumba yaufumu ino, atakwera magaleta ndi akavalo, iwowo pamodzi
ndi nduna zawo ndi anthu awo. 5 Koma ngati sumvera malamulo awa,
akutero Yehova, ndikulumbira pali Ine ndemwe kuti nyumba ino yaufumu
idzasanduka bwinja.’ ”

6 Pakuti zimene Yehova akunena za nyumba yaufumu ya mfumu ya ku
Yuda ndi izi:
“Ngakhale iwe uli ngati Giliyadi kwa Ine,
ngati msonga ya phiri la Lebanoni,
komabe ndidzakusandutsa chipululu,
ngati mizinda yopanda anthu.
7 Ndidzatuma anthu oti adzakuwononge,
munthu aliyense ali ndi zida zake,
ndipo adzadula mikungudza yako yokongola
nadzayiponya pa moto.

8 “Pamene anthu a mitundu ina adzadutsa pa mzinda umenewu
adzafunsana kuti, ‘Chifukwa chiyani Yehova wachita chinthu chotere pa
mzinda waukuluwu?’ 9 Ndipo yankho lake lidzakhala lakuti, ‘Chifukwa
anasiya pangano limene anapangana ndi Yehova Mulungu wawo ndipo
anapembedza ndi kutumikira milungu ina.’ ”
10 Musayilire mfumu Yosiya, musamuyimbire nyimbo womwalirayo;
m’malo mwake, mulire kwambiri chifukwa cha Yehowahazi amene wapita ku ukapolo,
chifukwa sadzabwerereranso
kapena kuonanso dziko lake lobadwira.
11 Pakuti zimene Yehova akunena za Yehowahazi mwana wa Yosiya,
amene anatenga mpando waufumu wa Yuda m’malo mwa abambo ake

koma n’kuwusiya ndi izi: “Iye sadzabwereranso. 12 Iyeyo adzafera ku
ukapoloko. Sadzalionanso dziko lino.”

13 “Tsoka kwa munthu womanga nyumba yake mopanda chilungamo,
womanga zipinda zake zosanja monyenga,
pogwiritsa ntchito abale ake mwathangata,
osawapatsa malipiro a ntchito yawo.
14 Munthuyo amati, ‘Ndidzadzimangira nyumba yayikulu
ya zipinda zikuluzikulu zam’mwamba.’
Kotero ndidzapanga mazenera akuluakulu,
ndi kukhomamo matabwa a mkungudza
ndi kukongoletsa ndi makaka ofiira.

15 “Kodi kukhala ndi nyumba ya mkungudza wambiri
zingachititse iwe kukhala mfumu?
Ganiza za abambo ako. Suja anali ndi zonse zakudya ndi zakumwa.
Abambo ako ankaweruza molungama ndi mosakondera,
ndipo zonse zinkawayendera bwino.
16 Iye ankateteza anthu osauka ndi osowa,
ndipo zonse zinkamuyendera bwino.
Kodi zimenezi sindiye tanthauzo la kudziwa Ine?”
akutero Yehova.
17 “Koma maso ako ndi mtima sizili penanso,
koma zili pa phindu lachinyengo,
pa zopha anthu osalakwa
ndi pa kuzunza ndi pakulamulira mwankhanza.”
18 N’chifukwa chake Yehova ponena za Yehoyakimu mwana wa Yosiya
mfumu ya ku Yuda akuti,
“Anthu sadzamulira maliro kapena kunena kuti,
‘Kalanga ine, m’bale wanga! Kalanga ine mlongo wanga!
Anthu ake sadzamulira maliro kuti,
Kalanga ine, mbuye wathu! Taonani ulemerero wake wapita!’
19 Adzayikidwa ngati bulu,
kuchita kumuguguza ndi kukamutaya
kunja kwa zipata za Yerusalemu.”

20 “Tsono inu anthu a ku Yerusalemu, pitani ku mapiri a Lebanoni kuti
mukalire mofuwula kumeneko,
mawu anu akamveke mpaka ku Basani.
Mulire mofuwula muli ku Abarimu
chifukwa abwenzi ako onse awonongeka.
21 Ndinakuchenjezani pamene munali pa mtendere.
Koma inu munati, ‘Sindidzamvera.’
Umu ndi mmene mwakhala mukuchitira kuyambira mukali aang’ono.
Simunandimvere Ine.
22 Mphepo idzakuchotserani abusa anu onse,
ndipo abwenzi anu adzatengedwa ku ukapolo.
Pamenepo mudzachita manyazi ndi kunyozedwa
chifukwa cha zoyipa zanu zonse.
23 Inu amene mumakhala m’nyumba ya ku Lebanoni,
amene munamanga nyumba zanu pakati pa mikungudza,
mudzabuwula kwambiri pamene zowawa zidzakugwerani,
zonga za mkazi pa nthawi yake yochira!

24 “Pali Ine wamoyo, akutero Yehova, ngakhale iwe, Yehoyakini mwana
wa Yehoyakimu mfumu ya ku Yuda, ukanakhala ngati mphete ya ku
dzanja langa lamanja, ndikanakuvula n’kukutaya. 25 Ndidzakupereka kwa
amene akufuna kukupha, amene iwe umawaopa. Ndidzakupereka kwa
Nebukadinezara, mfumu ya ku Babuloni ndi anthu ake. 26 Iwe pamodzi
ndi amayi ako amene anakubereka ndidzakupititsani ku dziko lachilendo.
Ngakhale inu simunabadwire kumeneko, komabe mudzafera komweko.
27 Simudzabwereranso ku dziko limene mudzafuna kubwerera.”
28 Kodi Yehoyakini wakhala ngati mbiya yonyozeka,
yosweka imene anthu sakuyifunanso?
Kodi n’chifukwa chake iye pamodzi ndi ana ake,
achotsedwa n’kutayidwa ku dziko limene iwo sakulidziwa?
29 Iwe dziko, dziko, dziko,
Imva mawu a Yehova!
30 Yehova akuti,
“Munthu ameneyu mumutenge ngati wopanda ana,
munthu amene sadzakhala wochita bwino pamoyo wake wonse,
pakuti palibe ndi mmodzi yemwe mwa zidzukulu zake zomwe zidzachita bwino.
Palibe amene adzathe kukhala pa mpando waufumu wa Davide
ndi kulamulira Yuda.”

# 23

*Nthambi Yolungama*

1 “Tsoka kwa abusa amene akuwononga ndi kubalalitsa nkhosa za
pabusa panga!” akutero Yehova. 2 N’chifukwa chake Yehova, Mulungu
wa Israeli, ponena za abusa amene akuweta anthu anga akuti, “Mwa-
balalitsa ndi kumwaza nkhosa zanga. Komanso simunazisamale bwino.
Choncho ndidzakulangani chifukwa cha machimo anu,” akutero Yehova.
3 “Pambuyo pake Ine mwini wakene ndidzasonkhanitsa nkhosa zanga
zotsala, kuzichotsa ku mayiko onse kumene ndinazibalalitsira ndi kuz-
ibweretsanso ku msipu wawo. Kumeneko zidzaswana ndi kuchulukana.
4 Ndidzazipatsa abusa amene adzaziweta, ndipo sizidzaopanso kapena
kuchita mantha, ndipo palibe imene idzasochera,” akutero Yehova.
5 Yehova akuti, “Masiku akubwera,
pamene ndidzaphukitsira Davide Nthambi yowongoka.
Imeneyi ndiye mfumu imene idzalamulira mwanzeru, mwachilungamo ndi mosakondera m’dziko.
6 Pa masiku a ulamuliro wake Yuda adzapulumuka
ndipo Israeli adzakhala pamtendere.
Dzina limene adzamutcha ndi ili:
Yehova ndiye Chilungamo Chathu.
7 Choncho, masiku akubwera,” akutero Yehova, “pamene anthu sadzane-
nanso polumbira kuti, ‘Pali Yehova wamoyo, amene anatulutsa Aisraeli ku
Igupto,’ 8 koma adzanena kuti, ‘Pali Yehova wamoyo, amene anatulutsa
zidzukulu za Israeli ku dziko lakumpoto ndi ku mayiko konse kumene
anawabalalitsira.’ Ndipo iwo adzawabweretsa ku dziko lawolawo.”

*Aneneri Onyenga*

9 Kunena za aneneri awa:
Mtima wanga wasweka;
m’nkhongono mwati zii.

Ndakhala ngati munthu woledzera,
ngati munthu amene wasokonezeka ndi vinyo,
chifukwa cha Yehova
ndi mawu ake opatulika.
10 Dziko ladzaza ndi anthu achigololo;
lili pansi pa matemberero.
Dziko lasanduka chipululu ndipo msipu wawuma.
Aneneri akuchita zoyipa
ndipo akugwiritsa ntchito mphamvu zawo molakwika.

11 "Mneneri ngakhale wansembe onse sapembedza Yehova.
Amachita zoyipa ngakhale m'nyumba yanga,"
akutero Yehova.
12 "N'chifukwa chake njira zawo zidzakhala zoterera;
adzawapirikitsira ku mdima
ndipo adzagwera kumeneko.
Adzaona zosaona
m'nthawi ya chilango chawo,"
akutero Yehova.

13 "Pakati pa aneneri a ku Samariya
ndinaona chonyansa ichi:
Ankanenera m'dzina la Baala
ndipo anasocheretsa anthu anga, Aisraeli.
14 Ndipo pakati pa aneneri a ku Yerusalemu
ndaonapo chinthu choopsa kwambiri:
amachita chigololo, amanena bodza
ndipo amalimbitsa mtima anthu ochita zoyipa.
Choncho palibe amene amasiya zoyipa zake.
Kwa Ine anthu onsewa
ali ngati a ku Sodomu ndi Gomora."
15 Choncho ponena za aneneriwa Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Ndidzawadyetsa zakudya zowawa
ndi kuwamwetsa madzi a ndulu,
chifukwa uchimo umene wafalikira m'dziko lonse
ndi wochokera kwa aneneri a ku Yerusalemuwa."
16 Koma Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Musamvere zimene aneneri amenewa akulosera kwa inu;
zomwe aloserazo n'zachabechabe.
Iwo akungoyankhula za masomphenya a m'mitima mwawo basi,
osati zochokera kwa Yehova.
17 Iwo amapita ndi kumakawuza amene amandinyoza Ine kuti,
'zinthu zidzakuyenderani bwino.'
Kwa iwo amene amawumirira kutsata zofuna za mitima yawo amakawawuza kuti,
'palibe choyipa chimene chidzakugwereni.' "
18 Ine ndikuti, "Koma ndani wa iwo amene anakhalapo mu msonkhano wa Yehova?
Ndani anaonapo kapena kumvapo mawu ake?
Ndani mwa iwo analabadirako za mawu ake ndi kuwamvera?
19 Taonani ukali wa Yehova
uli ngati chimphepo chamkuntho,
inde ngati namondwe.
Ndipo adzakantha mitu ya anthu oyipa.

20 Mkwiyo wa Yehova sudzaleka
mpaka atachita zonse zimene
anatsimikiza mu mtima mwake.
Mudzazizindikira bwino zimenezi
masiku akubwerawa."
21 Yehova anati, "Ine sindinatume aneneri amenewa,
komabe iwo athamanga uku ndi uku kulalikira uthenga wawo;
Ine sindinawayankhule,
komabe iwo ananenera.
22 Iwo akanakhala pa msonkhano wanga
ndiye kuti akanamayankhula mawu anga kwa anthu anga.
Komanso bwenzi atawachotsa anthu anga m'njira zawo zoyipa
kuti aleke machimo awo."

23 Yehova akuti, "Kodi ndimakhala Mulungu pokhapokha ndikakhala pafupi,
ndiye sindine Mulungu?
24 Kodi wina angathe kubisala
Ine osamuona?"
"Kodi Ine sindili ponseponse kumwamba ndi dziko lapansi?"
Akutero Yehova.
25 "Ndamva zimene aneneri akuyankhula. Iwo amalosera zabodza
m'dzina langa n'kumati, 'Ndalota! Ndalota!' 26 Kodi zabodzazi zidza-
khalabe m'mitima ya aneneriwa mpaka liti? Iwotu amalosera zonyenga
za m'mitima yawo. 27 Aneneriwa amakhulupirira kuti anthu anga
adzayiwala mawu anga akamamva za maloto awo amene amayankhulana
ngati mmene anachitira makolo awo popembedza Baala. 28 Mneneri
amene ali ndi maloto afotokoze malotowo. Koma iye amene ali ndi
mawu anga alalikire mawuwo mokhulupirika. Kodi phesi lingafanane ndi
chimanga? 29 Kodi suja mawu anga amatentha ngati moto? Suja mawu
anga amaphwanya monga ichitira nyundo kuphwanya miyala?" Akutero
Yehova.
30 Yehova akuti, "N'chifukwa chake, Ine ndikudana nawo aneneri
amene amaberana okhaokha mawu n'kumati mawuwo ndi a Yehova."
31 Yehova akuti, "Inde, Ine ndikudana ndi aneneri amene amakonda
kuyankhula zabodza n'kumanena kuti, 'Amenewa ndi mawu a Yehova.' "
32 Yehova akuti, "Ndithudi, Ine ndikudana ndi aneneri a maloto abodzawa.
Iwo amafotokoza malotowo n'kumasocheretsa anthu anga ndi bodza
lawo losachita nalo manyazilo, chonsecho Ine sindinawatume kapena
kuwalamula. Iwo sathandiza anthuwa ndi pang'ono pomwe," akutero
Yehova.

### *Uthenga Wabodza ndi Aneneri Abodza*

33 Yehova anawuza Yeremiya kuti, "Anthu awa, kapena mneneri,
kapenanso wansembe, akakufunsa kuti, 'Kodi uthenga wolemetsa wa
Yehova ukuti chiyani?' uwawuze kuti, 'Inuyo ndinu katundu wolemetsa
Yehova, ndipo adzakutayani.' 34 Ngati mneneri kapena wansembe
kapenanso munthu wina aliyense anena kuti, 'Uthenga wolemetsa wa
Yehova ndi uwu,' Ine ndidzalanga munthu ameneyo pamodzi ndi banja
lake. 35 Koma chimene aliyense wa inu azifunsa kwa mnzake kapena
m'bale wake ndi ichi: 'Kodi Yehova wayankha chiyani?' kapena
'Yehova wayankhula chiyani?' 36 Koma musanenenso kuti 'nawu uthenga
wolemetsa wa Yehova,' chifukwa mawu a munthu aliyense ndiwo uthenga

wa iye mwini, kotero kuti inu mumakhotetsa mawu a Mulungu wamoyo,
Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wathu. 37 Tsono iwe Yeremiya
udzamufunse mneneri kuti, 'Kodi Yehova wakuyankha chiyani?' kapena,
'Kodi Yehova wayankhula chiyani?' 38 Ngati mudzanena kuti, 'Nawu
uthenga wolemetsa wa Yehova,' ndiye tsono Yehova akuti, 'Popeza
mwagwiritsa ntchito mawu akuti: Nawu uthenga wolemetsa wa Yehova,
mawu amene ndinakuletsani kuti musawatchule, 39 ndiye kuti Ine ndidza-
kunyamulani ngati katundu n'kukuponyani kutali. Ndidzakuchotsani
pamaso panga, inuyo pamodzi ndi mzinda umene ndinakupatsani inu
ndi makolo anu. 40 Ndidzakunyozani mpaka muyaya. Ndidzakuchititsani
manyazi osayiwalika.' "

# 24

*Madengu Awiri a Nkhuyu*

1 Nebukadinezara, mfumu ya ku Babuloni anatenga ukapolo Yekoniya
mwana wa Yehoyakimu mfumu ya ku Yuda pamodzi ndi nduna zake,
anthu aluso ndi akatswiri a ku Yuda ndi kupita nawo ku Babuloni.
Pambuyo pake Yehova anandionetsa madengu awiri a nkhuyu atayikidwa
pa khomo pa Nyumba ya Yehova. 2 M'dengu limodzi munali nkhuyu
zabwino kwambiri, ngati nkhuyu zoyambirira kucha. M'dengu linalo
munali nkhuyu zoyipa kwambiri zosati n'kudya.

3 Yehova anandifunsa kuti, "Yeremiya, kodi ukuona chiyani?"

Ndinayankha kuti, "Ndikuona nkhuyu zabwino kwambiri ndi nkhuyu
zoyipa zosati n'kudya."

4 Tsono Yehova anandiwuza kuti, 5 "Ine Yehova, Mulungu wa Israeli
ndikuti, 'Anthu a ku Yuda amene ndinawachotsa ku malo ano n'kupita
nawo ku ukapolo ku dziko la Ababuloni ndikuwafanizira ndi nkhuyu
zabwinozi. 6 Ndidzaonetsesa kuti ndiwachitire zabwino ndipo ndidz-
abwera nawonso ku dziko lino. Ndidzawamanga osati kuwapasula;
ndidzawadzala osati kuwazula. 7 Ndidzawapatsa mtima woti andidziwe
kuti ndine Yehova. Adzakhala anthu anga ndipo Ine ndidzakhala Mulungu
wawo, chifukwa adzabwerera kwa Ine ndi mtima wawo wonse.

8 " 'Koma monga nkhuyu zoyipa zija, zomwe ndi zoyipa kwambiri zosati
n'kudya,' Yehova akuti, 'ndi mmene ndidzalangire Zedekiya mfumu ya ku
Yuda, nduna zake pamodzi ndi otsala a mu Yerusalemu, kaya adzakhala
ali m'dziko muno kapena m'dziko la Igupto. 9 Ndidzawasandutsa chinthu
chonyansa kwa maufumu onse a dziko lapansi, chinthu chonyozeka ndi
chopandapake, chinthu chochitidwa chipongwe ndi chotemberereredwa
kulikonse kumene ndidzawabalalitsira. 10 Ndidzawatumizira nkhondo,
njala ndi mliri mpaka atawonongedwa m'dziko limene ndinawapatsa iwo
ndi makolo awo.' "

# 25

*Zaka 70 za Ukapolo*

1 Yehova anayankhula ndi Yeremiya za anthu onse a ku Yuda m'chaka
chachinayi cha ufumu wa Yehoyakimu mwana wa Yosiya mfumu ya ku
Yuda, chimene chinali chaka choyamba cha ufumu wa Nebukadinezara
mfumu ya ku Babuloni. 2 Choncho mneneri Yeremiya anawuza anthu
onse a ku Yuda pamodzi ndi onse amene amakhala mu Yerusalemu kuti:
3 Kwa zaka 23, kuyambira chaka cha 13 cha ufumu wa Yosiya mwana wa

Amoni mfumu ya ku Yuda mpaka lero lino, Yehova wakhala akundipatsa
mauthenga ake ndipo ine ndakhala ndikuyankhula ndi inu kawirikawiri,
koma inu simunamvere.
4 Ndipo ngakhale Yehova kawirikawiri wakhala akukutumizirani atu-
miki ake onse, aneneri, inuyo simunamvere kapena kutchera khutu.
5 Aneneriwo ankanena kuti, “Ngati aliyense wa inu abwerere, kusiya njira
zake zoyipa ndi machitidwe ake oyipa, ndiye kuti mudzakhala m’dziko
limene Yehova anapereka kwa makolo anu kwamuyaya. 6 Musatsatire
milungu ina n’kuyitumikira ndi kuyipembedza. Musapute mkwiyo
wanga ndi mafano amene mwapanga ndi manja anu. Mukatero Ine
sindidzakuwonongani.
7 “Koma inu simunandimvere,” akutero Yehova, “ndipo munaputa
mkwiyo wanga ndi mafano amene munapanga ndi manja anu. Choncho
munadziwononga nokha.”
8 N’chifukwa chake Yehova Wamphamvuzonse akuti, “Chifukwa simu-
namvere mawu anga, 9 ndidzayitana mafuko onse akumpoto, pamodzi ndi
mtumiki wanga Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni,” akutero Yehova,
“ndipo adzathira nkhondo dziko lino ndi anthu ake pamodzi ndi mitundu
yonse ya anthu ozungulira dzikoli. Ndidzawawononga kwathunthu
ndi kuwasandutsa chinthu chochititsa mantha ndi chonyozeka, mpaka
muyaya. 10 Ndidzathetsa mfuwu wachimwemwe ndi wachisangalalo,
mawu a mkwati ndi mkwatibwi, phokoso la mphero ndi kuwala kwa
nyale. 11 Dziko lonse lidzakhala bwinja ndi chipululu, ndipo mitundu ina
idzatumikira mfumu ya ku Babuloni kwa 70.
12 “Koma zaka 70 zikadzatha, ndidzalanga mfumu ya ku Babuloni
pamodzi ndi anthu ake, chifukwa cha zolakwa zawo,” akutero Yehova,
“ndipo dziko lawo lidzakhala chipululu mpaka muyaya. 13 Ndidzachita
zinthu zonse zimene ndinayankhula zotsutsa dzikolo, zonse zimene
zalembedwa m’buku lino, ndiponso zonse zimene Yeremiya analosera
zotsutsa anthu amenewa. 14 Iwo eni adzakhala akapolo a anthu a mitundu
yochuluka ndi mafumu amphamvu. Ndidzawabwezera molingana ndi
zochita zawo ndi ntchito za manja awo.”

### *Chikho cha Ukali wa Mulungu*

15 Yehova, Mulungu wa Israeli, anandiwuza kuti, “Tenga chikho ichi
chodzaza ndi vinyo wa ukali wanga, ndipo ukamwetse anthu a mitundu
yonse kumene ndikukutuma. 16 Akadzamwa adzayamba kudzandira ndi
kuchita misala chifukwa cha nkhondo imene ndikuyitumiza pakati pawo.”
17 Choncho ine ndinatenga chikhocho m’dzanja la Yehova ndipo
ndinamwetsa mitundu yonse ya anthu kumene Iye ananditumako:
18 Ananditumа ku Yerusalemu ndi ku mizinda ya Yuda, kwa mafumu ake
ndi nduna zake kuti ndikawasandutse ngati bwinja ndi chinthu chochititsa
mantha ndi chonyozeka ndiponso chotembereredwa, monga mmene alili
lero lino. 19 Ananditumanso kwa Farao, mfumu ya ku Igupto, kwa atumiki
ake, nduna zake ndi kwa anthu ake onse, 20 ndi kwa anthu ena onse
a mitundu yachilendo; mafumu onse a ku Uzi; mafumu onse a Afilisti,
a ku Asikeloni, ku Gaza, ku Ekroni ndiponso kwa anthu a ku chigwa
chotsala cha Asidodi; 21 Edomu, Mowabu ndi Amoni. 22 Ananditumanso
kwa mafumu onse a ku Turo ndi ku Sidoni; kwa mafumu a kutsidya la
nyanja; 23 ku Dedani, ku Tema, ku Buzi ndi kwa onse ometa cham’mbali.
24 Ananditumanso kwa mafumu onse a ku Arabiya ndi mafumu onse

a anthu achilendo amene amakhala m'chipululu. 25 Ananditumu kwa
mafumu onse a ku Zimuri, Elamu ndi Mediya; 26 ndiponso kwa mafumu
onse a kumpoto, akufupi ndi kutali omwe, mafumu onse a dziko lapansi.
Ndipo potsiriza pake, idzamwenso ndi mfumu Sesaki.

27 "Ndipo uwawuze kuti, 'Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa
Israeli akuti: Imwani, ledzerani ndipo musanze, mugwe osadzukanso
chifukwa cha nkhondo imene ndikutumiza pakati panu.' 28 Koma ngati
akana kutenga chikhocho m'dzanja lako ndi kumwa, uwawuze kuti,
'Yehova Wamphamvuzonse akuti: Muyenera kumwa ndithu!' " 29 Taonani,
tsopano ndiyamba kulanga mzinda uno umene umadziwika ndi dzina
langa. Kodi inu muganiza kuti simudzalangidwa? Ayi, simudzapulumuka
chifukwa ndikutumiza nkhondo pa onse okhala pa dziko lapansi, akutero
Yehova Wamphamvuzonse.

30 "Tsopano iwe nenera mawu owatsutsa ndipo uwawuze kuti,
" 'Yehova adzabangula kumwamba;
mawu ake adzamveka ngati bingu kuchokera ku malo ake opatulika.
Adzabangula mwamphamvu kukalipira dziko lake.
Iye adzafuwula ngati anthu oponda mphesa,
kukalipira onse amene akukhala pa dziko lapansi.
31 Phokoso lalikulu lidzamveka mpaka kumalekezero a dziko lonse lapansi,
chifukwa Yehova adzazenga mlandu anthu a mitundu yonse;
adzaweruza mtundu wonse wa anthu
ndipo oyipa adzawapha ndi lupanga,' "
akutero Yehova.

32 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Taonani! Mavuto akuti akachoka
pa mtundu wina akukagwa pa mtundu wina;
mphepo ya mkuntho ikuyambira
ku malekezero a dziko."

33 Pa tsiku limenelo, onse ophedwa ndi Yehova adzangoti mbwee
ponseponse, pa dziko lonse lapansi. Palibe amene adzawalire kapena
kusonkhanitsa mitemboyo kuti ikayikidwe m'manda, koma idzakhala
mbwee ngati ndowe.

34 Khetsani misozi ndi kufuwula mwamphamvu, abusa inu;
gubudukani pa fumbi, inu atsogoleri a nkhosa.
Pakuti nthawi yanu yophedwa yafika;
mudzagwa ndi kuphwanyika ngati mbiya yabwino kwambiri.
35 Abusa adzasowa kothawira,
atsogoleri a nkhosa adzasowa malo opulumukira.
36 Imvani kulira kwa abusa,
atsogoleri a nkhosa akulira,
chifukwa Yehova akuwononga msipu wawo.
37 Makola awo a nkhosa amene anali pamtendere adzasanduka bwinja
chifukwa cha mkwiyo woopsa wa Yehova.
38 Ngati mkango, Yehova wasiya phanga lake,
pakuti dziko lawo lasanduka chipululu
chifukwa cha nkhondo ya owazunza
ndiponso chifukwa cha mkwiyo woopsa wa Yehova.

# 26

*Yeremiya Amangidwa*

[1] Yehoyakimu, mwana wa Yosiya mfumu ya ku Yuda atayamba ku-
lamulira, Yehova anayankhula ndi Yeremiya kuti, [2] "Kayime m'bwalo
la Nyumba ya Yehova. Ndipo ukayankhule kwa anthu onse okhala
m'mizinda ya ku Yuda amene amabwera kudzapembedza ku Nyumba ya
Yehova. Ukawawuze zonse zomwe ndakulamula; usakasiyeko ndi mawu
amodzi omwe. [3] Mwina mwake adzamvera, ndipo aliyense adzatembe-
nuka kuleka njira yake yoyipa. Ndiye ine ndidzaleka osapatsa chilango
chimene ndinakonzekera kuti ndiwalange nacho chifukwa cha ntchito
zawo zoyipa. [4] Ukawawuze kuti, 'Yehova akuti: Ngati simundimvera Ine
ndi kuleka kutsatira malamulo anga, amene ndakupatsani, [5] ndipo ngati
simumvera mawu a atumiki anga, aneneri amene ndakhala ndikukutu-
mizirani, ngakhale kuti simunawamvere, [6] ndiye kuti Ine ndidzasandutsa
Nyumba ino kukhala ngati Silo ndipo mzinda uno udzakhala chinthu
chotembereredwa pakati pa mitundu yonse ya pa dziko lapansi.' "

[7] Ansembe, aneneri ndi anthu onse anamva Yeremiya akuyankhula
mawu amenewa m'Nyumba ya Yehova. [8] Yeremiya atangotsiriza
kuwawuza anthu aja zonse zimene Yehova anamulamula kuti ayankhule,
ansembe, aneneri pamodzi ndi anthu onse anamugwira ndipo anati,
"Uyenera kuphedwa! [9] Chifukwa chiyani walosera m'dzina la Yehova
kuti Nyumba ino idzakhala ngati Silo ndipo mzinda uno udzakhala
wopanda anthu ngati chipululu?" Anthu onse anamuzungulira Yeremiya
m'Nyumba ya Yehova.

[10] Koma nduna za ku Yuda zitamva zomwe zinachitikazi, zinanya-
muka kuchokera ku nyumba yaufumu kupita ku Nyumba ya Yehova,
nakakhala pamalo pawo, pa Chipata Chatsopano cha Nyumba ya Yehova.
[11] Pamenepo ansembe ndi aneneri anawuza ndunazo pamodzi ndi anthu
onse kuti, "Munthu uyu ayenera kuphedwa chifukwa amalosera zoyipira
mzinda uno. Inu mwadzimvera nokha zimenezi!"

[12] Ndipo Yeremiya anawuza nduna zija ndi anthu onse kuti, "Yehova
ananditumа kunenera mawu onse amene mwawamva otsutsa Nyumba
ino ndi mzinda uno. [13] Tsopano konzani njira zanu ndi zochita zanu ndipo
mverani Yehova Mulungu wanu. Mukatero ndiye kuti Yehova adzaleka
osakupatsani chilango chimene ankati akupatseni. [14] Kunena za ine, ndili
m'manja mwanu; mundichite chilichonse chimene mukuganiza kuti ndi
chabwino ndi choyenera. [15] Komatu dziwani kuti ngati mundipha, inu
pamodzi ndi mzinda uno ndi onse amene amakhala muno, mudzapala-
mula mlandu wokhetsa magazi a munthu wosalakwa. Ndithudi Yehova
ananditumа kuti ndidzayankhule mawu onsewa inu mukumva."

[16] Pamenepo ndunazo pamodzi ndi anthu onse anawuza ansembe ndi
aneneri kuti, "Munthu uyu sayenera kuphedwa! Pakuti wayankhula kwa
ife m'dzina la Yehova Mulungu wathu."

[17] Akuluakulu ena a m'dzikomo anayimirira ndi kuwuza gulu lonse la
anthu kuti, [18] "M'masiku a Hezekiya mfumu ya ku Yuda, Mika wa ku
Moreseti ankalosera. Iye ankawuza anthu kuti Yehova Wamphamvuzonse
akuti,

" 'Ziyoni adzatipulidwa ngati munda,
Yerusalemu adzasanduka bwinja,
ndipo phiri la Nyumba ya Mulungu lidzasanduka nkhalango yowirira.'

[19] Kodi Hezekiya mfumu ya ku Yuda ndi anthu onse anamupha amene uja?
Kodi suja mfumu inaopa Yehova ndi kupempha kuti ayikomere mtima?
Ndipo suja Yehova anasintha maganizo ake n'kuleka kuwalanga monga
m'mene anakonzera? Ifetu tikudziyitanira tsoka lalikulu!"

[20] (Panalinso munthu wina, Uriya mwana wa Semaya wa ku Kiriati-
Yeyarimu, amene ankalosera m'dzina la Yehova. Iyeyu analosera za
mzinda uno ndi dziko lino monga mmene wachitira Yeremiya. [21] Mfumu
Yehoyakimu, ankhondo ake onse ndi nduna zake anamva mawu akewo,
ndipo anafuna kumupha. Koma Uriya atamva zimenezi, anachita mantha
nathawira ku Igupto. [22] Komabe Mfumu Yehoyakimu anatuma Elinatani
mwana wa Akibori pamodzi ndi anthu ena, ku Igupto. [23] Iwo anaka-
mutenga Uriya ku Igupto kuja nabwera naye kwa Mfumu Yehoyakimu.
Iye anamupha ndi lupanga ndipo mtembo wake anakawutaya ku manda
a anthu wamba).
[24] Koma Ahikamu mwana wa Safani ndiye anateteza Yeremiya, motero
sanamupereke kwa anthu kuti amuphe.

# 27

*Yuda Adzatumikira Nebukadinezara*

[1] Zedekiya mwana wa Yosiya, mfumu ya ku Yuda, atangoyamba
kulamulira, Yehova anawuza Yeremiya kuti, [2] "Tenga zingwe zomangira
ndi mitengo ya goli ndipo uzimangirire m'khosi mwako. [3] Tsono utumize
uthenga kwa mafumu a Edomu, Mowabu, Amoni, Turo ndi Sidoni
kudzera mwa amithenga amene abwera ku Yerusalemu kwa Zedekiya,
mfumu ya Yuda. [4] Uwapatse uthenga wokapereka kwa ambuye awo
ndipo uwawuze kuti: Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli
akuti, 'Mukawuze ambuye anu kuti: [5] Ndi mphamvu zanga ndi dzanja
langa lamphamvu ndinalenga dziko lapansi ndi anthu ake onse pamodzi
ndi nyama zili m'menemo, ndipo ndimalipereka kwa aliyense amene
ndikufuna. [6] Tsopano ndidzapereka mayiko anu onse kwa mtumiki
wanga Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni. Ndamupatsanso nyama
zakuthengo zonse kuti zimutumikire. [7] Anthu a mitundu yonse adzamutu-
mikira iyeyo, mwana wake ndi chidzukulu chake mpaka nthawi itakwana
yoti dziko lake liwonongedwe. Pamenepo mitundu yambiri ndi mafumu
amphamvu adzamugonjetsa.
[8] " 'Koma ngati anthu a mtundu wina uliwonse kapena ufumu wina
uliwonse adzakana kutumikira Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni
kapena kusenza goli lake, Ine ndidzalanga mtundu umenewo ndi lupanga,
ndi njala ndi mliri, akutero Yehova, mpaka nditawapereka m'manja
mwake kotheratu. [9] Choncho musamvere aneneri anu, owombeza
anu, otanthauza maloto anu, amawula anu kapena amatsenga anu
akamakuwuzani kuti, 'Simudzatumikira mfumu ya ku Babuloni.' [10] Iwo
akukuloserani zabodza kotero kuti adani adzakuchotsani m'dziko lanu
n'kupita nanu ku dziko lakutali. Ndidzakupirikitsani ndi kukuwonongani
kotheratu. [11] Koma ngati mtundu wina uliwonse udzagonjera mfumu ya
ku Babuloni ndi kuyitumukira, ndidzawusiya kuti ukhale m'dziko lake
kuti uzilima ndi kukhalamo, akutero Yehova.' "
[12] Uthenga womwewu ndinawuzanso Hezekiya mfumu ya Yuda. Nd-
inati, "Gonjerani mfumu ya ku Babuloni. Itumikireni iyoyo pamodzi
ndi anthu ake ndipo mudzakhala ndi moyo. [13] Nanga inu ndi an-
thu anu, muferenji ndi lupanga, ndi njala, ndi mliri, zimene Yehova
waopsezera mtundu wina uliwonse umene sudzatumikira mfumu ya
ku Babuloni? [14] Musamvere mawu a aneneri akamakuwuzani kuti,
'Simudzatumikira mfumu ya ku Babuloni,' chifukwa zimene akuku-
loseranizo n'zabodza. [15] Sindinawatume ngakhale iwo akulosera m'dzina

langa. N’chifukwa chake, ndidzakupirikitsani ndipo mudzawonongeka
kotheratu, inu pamodzi ndi aneneri amene akunenera zabodza kwa inu.”
16 Kenaka ndinawuza ansembe pamodzi ndi anthu ena onse kuti,
“Yehova akuti: Musamvere aneneri amene akumanena kuti, ‘Posached-
wapa ziwiya za m’Nyumba ya Yehova zibwera kuchokera ku Babuloni.’
Iwowo akunenera zabodza kwa inu. 17 Musawamvere. Tumikirani mfumu
ya ku Babuloni, ndipo mudzakhala ndi moyo. Mzindawu usandukirenji
bwinja? 18 Ngati iwo ndi aneneri ndipo ali ndi mawu a Yehova,
apempheretu kwa Yehova Wamphamvuzonse kuti ziwiya zimene zatsala
m’Nyumba ya Yehova ndi m’nyumba ya mfumu ya Yuda ndiponso mu
Yerusalemu zisatengedwe kupita ku Babuloni. 19 Pakuti Yehova akunena
za zipilala, za mbiya ya madzi, maphaka ndi ziwiya zina zimene zatsala
mu Yerusalemu. 20 Izi ndi zimene Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni
sanatenge pamene anatenga ukapolo Yekoniya mwana wa Yehoyakimu
mfumu ya Yuda kupita ku Babuloni kuchokera ku Yerusalemu, pamodzi
ndi anthu olemekezeka a ku Yuda ndi a ku Yerusalemu. 21 Inde, Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli, akunena za zinthu zimene
zinatsala m’Nyumba ya Yehova ndi m’nyumba ya mfumu ya Yuda ndi mu
Yerusalemu kuti, 22 ‘Zidzatengedwa kupita ku Babuloni ndipo zidzakhala
kumeneko mpaka tsiku limene ndidzawakumbukirenso,’ akutero Yehova.
‘Pamenepo ndidzazitenganso ndi kuzibwezanso ku malo ano.’ ”

# 28

*Hananiya Atsutsana ndi Yeremiya*

1 Chaka chomwecho mwezi wachisanu wa chaka chachinayi, poyam-
birira pa ulamuliro wa Zedekiya mfumu ya Yuda, mneneri Hananiya
mwana wa Azuri, amene amachokera ku Gibiyoni, anandiwuza ine
m’Nyumba ya Yehova pamaso pa ansembe ndi anthu onse kuti, 2 “Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli, akuti, ‘Ndidzathyola goli la
mfumu ya ku Babuloni. 3 Pasanathe zaka ziwiri ndidzabweretsa pa
malo ano ziwiya zonse za ku Nyumba ya Yehova zimene Nebukadinezara
mfumu ya ku Babuloni anazichotsa pa malo pano ndi kupita nazo ku
Babuloni. 4 Ndidzabweretsanso pa malo pano Yekoniya mwana wa Yehoy-
akimu mfumu ya Yuda pamodzi ndi akapolo ena onse ochokera ku Yuda
amene anapita ku Babuloni,’ akutero Yehova, ‘chifukwa ndidzathyola goli
la mfumu ya ku Babuloni.’ ”

5 Pamenepo mneneri Yeremiya anayankha mneneri Hananiya pamaso
pa ansembe ndi anthu onse amene anasonkhana m’Nyumba ya Yehova.
6 Anati, “Ameni! Yehova achitedi zomwezo! Yehova akwaniritse mawu
amene waloserawo. Iye abweretsenso pa malo pano ziwiya za m’Nyumba
ya Yehova ndi akapolo onse kuchokera ku Babuloni. 7 Komabe, tamvera
zimene nditi ndikuwuze iweyo pamodzi ndi anthu onse: 8 Kunali aneneri
kalelo, ine ndi iwe tisanabadwe. Iwowa analosera za nkhondo, mavuto ndi
mliri kuti zidzagwera mayiko ambiri ndi maufumu amphamvu. 9 Koma
mneneri amene amalosera zamtendere adzadziwika kuti ndi woona ndi
kuti watumidwa ndi Yehova ngati zimene wanenera zachitikadi.”

10 Pamenepo mneneri Hananiya anachotsa goli m’khosi mwa mneneri
Yeremiya nalithyola, 11 ndipo anawuza anthu onse kuti, “Yehova akuti,
‘Umu ndi mmene ndidzathyolere goli la Nebukadinezara mfumu ya ku

Babuloni m'khosi mwa anthu a mitundu yonse pasanathe zaka ziwiri.' "
Zitatero, mneneri Yeremiya anachoka.
12 Patapita nthawi pang'ono, mneneri Hananiya atathyola goli m'khosi
mwa mneneri Yeremiya, Yehova anawuza Yeremiya kuti, 13 "Pita, kawuze
mneneri Hananiya kuti, 'Yehova akuti: Iwe wathyola goli lamtengo,
m'malo mwake Ine ndidzayika goli lachitsulo. 14 Yehova Wamphamvu-
zonse, Mulungu wa Israeli akuti: Ndidzayika goli lachitsulo m'khosi mwa
anthu a mitundu yonseyi kuti atumikire Nebukadinezara mfumu ya ku
Babuloni, ndipo iwo adzamutumikiradi. Ndipo ndamupatsanso ulamuliro
ngakhale pa nyama zakuthengo.' "
15 Ndipo mneneri Yeremiya anawuza mneneri Hananiya kuti, "Tamvera,
Hananiya! Iweyo Yehova sanakutume, koma iwe wanyenga anthuwa
kuti akhulupirire zabodza. 16 N'chifukwa chake Yehova akuti, 'Ndatsala
pang'ono kukuchotsa pa dziko lapansi. Iwe ufa chaka chino chisanathe,
chifukwa wakhala ukulalikira zowukira Yehova.' "
17 M'mwezi wachisanu ndi chiwiri wa chaka chomwecho, mneneri
Hananiya anamwaliradi.

# 29

*Kalata Yolembera Anthu a ku Ukapolo*

1 Yeremiya anatumiza kalata kuchokera ku Yerusalemu kupita kwa
akuluakulu amene anali ku ukapolo, ndiponso kwa ansembe, aneneri
pamodzi ndi anthu onse amene Nebukadinezara anawatenga ku
Yerusalemu kupita nawo ku ukapolo ku Babuloni. 2 Zimenezi zinachitika
mfumu Yekoniya, amayi a mfumu, nduna za mfumu ndiponso atsogoleri
a ku Yuda ndi a ku Yerusalemu, anthu aluso ndi amisiri atatengedwa ku
Yerusalemu kupita ku ukapolo. 3 Yeremiya anapatsira kalatayo Eleasa
mwana wa Safani ndi Gemariya mwana wa Hilikiya, amene Zedekiya
mfumu ya Yuda anawatumiza kwa Mfumu Nebukadinezara ku Babuloni.
M'kalatamo analembamo kuti:

4 Anthu onse amene anatengedwa ukapolo kuchokera ku Yerusalemu
kupita ku Babuloni, Yehova akuwawuza kuti, 5 "Mangani nyumba
ndipo muzikhalamo. Limani minda ndipo mudye zipatso zake.
6 Kwatirani ndipo mubereke ana aamuna ndi aakazi. Ana anu aamuna
muwasankhire akazi ndipo muwasankhire amuna ana anu aakaziwo,
kuti nawonso abale ana aamuna ndi aakazi. Muchulukane kumeneko.
Chiwerengero chanu chisachepe. 7 Ndiponso muzifunafuna mtendere
ndi ubwino wa mzinda umene ndinakupirikitsirani ku ukapoloko.
Muzipempherera mzindawo kwa Yehova, kuti zikuyendereni bwino."
8 Inde, Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akunena kuti,
"Musalole kuti aneneri ndi owombeza amene ali pakati panu akun-
yengeni. Musamvere maloto awo. 9 Iwo akunenera zabodza kwa inu
m'dzina langa ngakhale Ine sindinawatume," akutero Yehova.

10 Yehova akuti, "Zaka 70 za ku Babuloni zikadzatha, ndidzabw-
era kudzakuchitirani zabwino zonse zimene ndinakulonjezani zija,
ndipo ndidzakubwezerani ku malo ano. 11 Pakuti Ine ndikudziwa
zimene ndinakukonzerani," akutero Yehova, "ndimalingalira zabwino
zokhazokha za inu osati zoyipa, ayi. Ndimalingalira zinthu zokupat-
sani chiyembekezo chenicheni pa za m'tsogolo. 12 Nthawi imeneyo
mudzandiyitana, ndi kunditama mopemba ndipo ndidzakumverani.
13 Mudzandifunafuna ndipo mudzandipeza. Mukadzandifuna ndi

mtima wanu wonse [14] mudzandipezadi," akutero Yehova, "ndipo
ndidzakubwezerani zabwino zanu. Ndidzakusonkhanitsani kuchokera
ku mayiko onse ndi kumalo konse kumene munali," akutero Yehova,
"ndipo ndidzakubweretsani kumalo kumene munali ndisanakuchotseni
kukupititsani ku ukapolo."

[15] Inu mumati, "Yehova watiwutsira aneneri athu ku Babuloni,"
[16] koma zimene Yehova akunena za mfumu imene ikukhala pa mpando
waufumu wa Davide pamodzi ndi anthu onse amene anatsala mu
mzinda muno, abale anu amene sanapite nanu ku ukapolo ndi izi,
[17] Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Ndidzawapha ndi nkhondo, njala
ndi mliri ndipo ndidzawasandutsa ngati nkhuyu zowola kwambiri,
zosati n'kudya. [18] Ndidzawalondola ndi lupanga, njala ndi mliri
ndipo ndidzawasandutsa chinthu chonyansa kwa anthu amayiko onse
a pa dziko lapansi. Adzakhala otembereredwa, ochititsa mantha,
onyozeka ndiponso ochitidwa chipongwe pakati pa anthu a mitundu
yonse kumene ndawapirikitsirako. [19] Zidzatero chifukwa sanamvere
mawu anga amene ndinkawatumizira kudzera mwa atumiki anga,
aneneri. Ngakhale inu amene muli ku ukapolo simunamverenso,"
akutero Yehova.

[20] Choncho, imvani mawu a Yehova, inu akapolo nonse amene ndi-
nakuchotsani mu Yerusalemu ndi kukupititsani ku Babuloni. [21] Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti zokhudza Ahabu mwana
wa Kolaya ndi Zedekiya mwana wa Maseya, amene akulosera zabodza
kwa inu m'dzina langa: "Taonani ndidzawapereka kwa Nebukadinezara
mfumu ya ku Babuloni, ndipo adzawapha inu mukupenya. [22] Chifukwa
cha anthu awiriwo, akapolo onse ochokera ku Yuda amene ali ku
Babuloni adzagwiritsa ntchito mawu awa potemberera: 'Yehova achite
nawe monga mmene anachitira ndi Zedekiya ndi Ahabu, amene mfumu
ya ku Babuloni inawatentha.' [23] Pakuti anthu amenewa achita zoyipa
kwambiri mu Israeli; achita chigololo ndi akazi a eni ake ndipo m'dzina
langa ankayankhula zabodza zimene sindinawawuze kuti atero. Ine
ndikuzidziwa ndipo ndine mboni ya zimenezi," akutero Yehova.

### *Kalata ya Semaya*

[24] Ukamuwuze Semaya wa ku Nehelamu kuti, [25] "Yehova Wamphamvu-
zonse, Mulungu wa Israeli akuti: Iwe unatumiza kalata m'dzina lako kwa
anthu onse a mu Yerusalemu, kwa Zefaniya mwana wa wansembe Maseya,
ndi kwa ansembe onse. Unalemba mu kalatayo kuti, [26] 'Yehova waku-
sankha kukhala wansembe m'malo mwa Yehoyada kuti ukhale wamkulu
woyang'anira Nyumba ya Yehova. Munthu aliyense wamisala amene
akudziyesa kuti ndi mneneri uzimuponya m'ndende ndi kumuveka goli
lachitsulo. [27] Nanga tsono chifukwa chiyani simunamuchitire zimenezi
Yeremiya wa ku Anatoti, amene amakhala ngati mneneri pakati panu?
[28] Yeremiyayo watitumizira uthenga uwu kuno ku Babuloni: Ukapolo
wanu ukhala wa nthawi yayitali. Choncho mangani nyumba ndipo
muzikhalamo; limani minda ndipo mudye zipatso zake.' "

[29] Koma wansembe Zefaniya anayiwerenga kalatayo pamaso pa mneneri
Yeremiya. [30] Ndipo Yehova anawuza Yeremiya kuti, [31] "Tumiza uthenga
uwu kwa akapolo onse: 'Yehova akuti zokhudza Semaya wa ku Nehelamu:
Semaya wakuloserani, ngakhale kuti Ine sindinamutume, ndipo wakun-
yengani kuti muzikhulupirira bodza. [32] N'chifukwa chake Ine Yehova
ndikuti: M'banja lakelo sipadzakhala munthu pakati pa mtundu uno wa

anthu amene adzaone zinthu zabwino zimene ndidzachitira anthu anga chifukwa analalika zondiwukira,' " akutero Yehova.

# 30

*Kubwezeretsedwa kwa Israeli*

1 Yehova anawuza Yeremiya kuti, 2 "Ine Yehova, Mulungu wa Israeli
ndikuti, 'Lemba m'buku mawu onse amene ndakuwuza. 3 Nthawi
ikubwera pamene ndidzachotse anthu anga, Israeli ndi Yuda kuchokera ku ukapolo ndi kuwabwezera dziko limene ndinapatsa makolo awo,' akutero Yehova."

4 Nawa mawu amene Yehova anayankhula ndi anthu a ku Israeli ndi
Yuda: 5 "Yehova akuti:

"Ndamva kulira chifukwa cha nkhawa,
ndamva kulira kwa mantha popeza palibe mtendere.
6 Tsono khalani pansi ndi kudzifunsa kuti:
Kodi munthu wamwamuna angathe kubereka mwana?
Nanga n'chifukwa chiyani ndikuona munthu aliyense wamwamuna
atagwira manja ake pa mimba pake ngati mayi pa nthawi yake yochira?
Chifukwa chiyani nkhope iliyonse ili yakugwa?
7 Mayo ine! Tsiku limeneli ndi lalikulu kwambiri!
Sipadzakhala lina lofanana nalo.
Idzakhala nthawi ya masautso kwa Yakobo,
koma adzapulumuka ku masautsowo."

8 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Pa tsiku limenelo,
ndidzathyola goli la ukapolo m'khosi mwawo
ndipo ndidzadula zingwe zowamanga;
Aisraeli sadzakhalanso akapolo a alendo.
9 M'malo mwake, adzatumikira Yehova Mulungu wawo
ndiponso Davide mfumu yawo,
amene ndidzawasankhira.

10 " 'Tsono usachite mantha, iwe mtumiki wanga Yakobo;
usade nkhawa, iwe Israeli,'
akutero Yehova.
'Ndithu ndidzakupulumutsa kuchokera ku dziko lakutali,
zidzukulu zako kuchokera ku dziko la ukapolo wawo.
Yakobo adzabwerera ndipo adzakhala modekha pa mtendere,
ndipo palibe amene adzamuchititsa mantha.
11 Ine ndili nanu ndipo ndidzakupulumutsani,'
akutero Yehova.
'Ngakhale ndidzawononga kotheratu mitundu yonse ya anthu
kumene ndinakubalalitsirani,
koma inu sindidzakuwonongani kotheratu.
Sindidzakulekani kuti mukhale osalangidwa.
Koma ndidzakulangani mwachilungamo.' "

12 Yehova akuti,
"Chilonda chanu n'chosachizika,
bala lanu ndi lonyeka.
13 Palibe amene angathe kukutetezani pa mlandu wanu,
palibe chiyembekezo choti inu n'kuchira,

palibe mankhwala ochiritsa inu.
14 Abwenzi anu onse akuyiwalani;
sasamalanso za inu.
Ndakukanthani ngati mmene mdani akanachitira.
Ndipo ndakulangani mwa nkhanza,
chifukwa machimo anu ndi ambiri,
ndipo kulakwa kwanu ndi kwakukulu.
15 Chifukwa chiyani mukulira nacho chilonda chanu?
Bala lanu silingapole ayi.
Ine ndakuchitani zimenezi chifukwa machimo anu ndi ambiri
ndipo kulakwa kwanu n'kwakukulu.

16 "Tsono onse amene anakuwononganani, nawonso adzawononongedwa;
adani anu onse adzapita ku ukapolo.
Iwo amene anafunkha zinthu zanu, zinthu zawo zidzafunkhidwanso;
onse amene anakusakazani nawonso adzasakazidwa.
17 Ndidzachiza matenda anu
ndi kupoletsa zilonda zanu,
akutero Yehova,
'chifukwa mukutchedwa anthu otayika.
Amati, ndi anthu a ku Ziyoni awa amene alibe wowasamala.' "
18 Yehova akuti,
"Ndidzabwera nalo banja la Yakobo ku dziko lawo
ndipo ndidzachitira chifundo malo ake okhalamo;
mzinda wa Yerusalemu udzamangidwanso pa bwinja pake,
nyumba yaufumu idzamangidwanso pa malo pake penipeni.
19 Anthuwo adzayimba nyimbo zoyamika Yehova
ndipo kudzamveka phokoso lachisangalalo.
Ndidzawachulukitsa,
ndipo chiwerengero chawo sichidzatsika;
ndidzawapatsa ulemerero,
ndipo sadzanyozedwanso.
20 Ana awo adzakhalanso monga mmene analili kale,
ndipo gulu lawo ndidzalikhazikitsa pamaso panga;
ndidzalanga onse owazunza.
21 Mtsogoleri wawo adzakhala mmodzi mwa iwo.
Wodzawalamulira adzachokera pakati pawo.
Choncho ndidzawakokera kufupi ndi Ine ndipo iye adzandiyandikira.
Ndani angalimbe mtima payekha kuyandikana nane
popanda kuyitanidwa?"
akutero Yehova.
22 "Choncho inu mudzakhala anthu anga,
ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wanu."

23 Taonani ukali wa Yehova wowomba
ngati mphepo ya mkuntho.
Mphepo ya namondwe
ikuwomba pa mitu ya anthu oyipa.
24 Mkwiyo woopsa wa Yehova sudzachoka
mpaka atakwaniritsa zolinga
za mu mtima mwake.
Mudzamvetsa zimenezi
masiku akubwerawo.

# 31

1 “Pa nthawi imeneyo,” akutero Yehova, “Ndidzakhala Mulungu wa
mafuko onse a Israeli, ndipo iwo adzakhala anthu anga.”
2 Yehova akuti,
“Anthu amene anapulumuka ku nkhondo
ndinawakomera mtima m’chipululu;
pamene Aisraeli ankafuna kupumula.”
3 Ine ndinawaonekera ndili chapatali ndipo ndinati,
“Ine ndakukondani ndi chikondi chopanda malire.
N’chifukwa chake ndipitiriza kukukondani.
4 Ndidzakusamaliraninso, inu anthu a Israeli;
mudzasangalala poyimba tizitoliro tanu,
ndipo mudzapita kukavina nawo
anthu ovina mwachimwemwe.
5 Mudzalimanso minda ya mpesa
pa mapiri a Samariya;
alimi adzadzala mphesa
ndipo adzadya zipatso zake.
6 Lidzafika tsiku pamene alonda adzafuwula
pa mapiri a Efereimu nati,
‘Tiyeni tipite ku Ziyoni,
kwa Yehova Mulungu wathu.’ ”
7 Yehova akuti,
“Imbani mosangalala chifukwa cha Yakobo,
fuwulani chifukwa cha mtundu wopambana mitundu yonse.
Matamando anu amveke, ndipo munene kuti,
‘Yehova wapulumutsa anthu ake
otsala a Israeli.’
8 Taonani, ndidzabwera nawo kuchokera ku dziko la kumpoto,
ndidzawasonkhanitsa kuchokera ku malekezero a dziko lapansi.
Anthu osaona, olumala, amayi oyembekezera
ndi amene ali pa nthawi yawo yochira adzabwera nawo pamodzi.
Chidzakhala chikhamu cha anthu obwerera kuno.
9 Adzabwera akulira;
koma Ine ndikuwatonthoza mtima, ndidzawaperekeza.
Ndidzawatsogolera ku mitsinje yamadzi
m’njira yosalala mmene sadzapunthwamo.
Chifukwa ndine abambo ake a Israeli,
ndipo Efereimu ndi mwana wanga woyamba.

10 “Imvani mawu a Yehova inu anthu a mitundu ina;
lalikirani mawuwa kwa anthu a mayiko akutali a m’mbali mwa nyanja;
‘Iye amene anabalalitsa Israeli adzawasonkhanitsanso
ndipo adzayang’anira nkhosa zake ngati m’busa.’
11 Pakuti Yehova wawombola fuko la Yakobo
anawapulumutsa m’dzanja la anthu owaposa mphamvu.
12 Anthuwo adzabwera akuyimba mofuwula pa mapiri a Ziyoni;
adzasangalala ndi zinthu zabwino zochokera kwa Yehova.
Zinthu zabwinozo ndi izi: tirigu, vinyo watsopano ndi mafuta,
ana ankhosa ndi ana ang’ombe.
Iwo adzakhala ngati munda wothiriridwa bwino,
ndipo sadzamvanso chisoni.

13 Pamenepo anamwali adzavina ndi kusangalala.
Anyamata ndi okalamba nawonso adzasangalala.
Kulira kwawo ndidzakusandutsa chisangalalo;
ndidzawasangalatsa n'kuchotsa chisoni chawo.
14 Ansembe ndidzawadyetsa chakudya chabwino,
ndipo anthu anga adzakhuta ndi zabwino zanga,"
akutero Yehova.
15 Yehova akuti,
"Kulira kukumveka ku Rama,
kulira kwakukulu,
Rakele akulirira ana ake.
Sakutonthozeka
chifukwa ana akewo palibe."
16 Yehova akuti,
"Leka kulira
ndi kukhetsa misozi
pakuti udzalandira mphotho ya ntchito yako,"
akutero Yehova.
"Iwo adzabwerako ku dziko la adani.
17 Tsono chiyembekezo chilipo pa zam'tsogolo,"
akutero Yehova.
"Ana ako adzabwerera ku dziko lawo.

18 "Ndithu ndamva Efereimu akubuuwula kuti,
'Ife tinali ngati ana ang'ombe osamva.
Koma inu mwatiphunzitsa kumvera.
Mutibweze kuti tithe kubwerera,
chifukwa ndinu Yehova Mulungu wanga.
19 Popeza tatembenuka mtima,
ndiye tikumva chisoni;
popeza tazindikira
ndiye tikudziguguda pachifukwa.
Tachita manyazi ndipo tanyazitsidwa
chifukwa tinachimwa paubwana wathu.'
20 Kodi Efereimu si mwana wanga wokondedwa,
mwana amene Ine ndimakondwera naye?
Ngakhale nthawi zambiri ndimamudzudzula,
ndimamukumbukirabe.
Kotero mtima wanga ukumufunabe;
ndimamumvera chifundo chachikulu kwambiri,"
akutero Yehova.

21 "Muyike zizindikiro za mu msewu;
muyimike zikwangwani.
Yang'anitsitsani msewuwo,
njira imene mukuyendamo.
Bwerera, iwe namwali wa Israeli,
bwerera ku mizinda yako ija.
22 Udzakhala jenkha mpaka liti,
iwe mwana wa mkazi wosakhulupirika?
Yehova walenga chinthu chatsopano pa dziko lapansi; mkazi ndiye tsopano aziteteza mwamuna."

23 Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti, “Ndikadzab-
wera nawo anthuwa kuchokera ku ukapolo, anthu a m’dziko la Yuda
ndi amene akukhala m’mizinda yake adzayankhulanso mawu akuti,
‘Yehova akudalitse, iwe malo achilungamo, iwe phiri lopatulika.’ 24 Anthu
adzakhala ku Yuda ndi ku mizinda yake pamodzi ndi alimi ndi oweta
nkhosa. 25 Ndidzatsitsimutsa anthu otopa ndipo ndidzadyetsa anthu
anjala.”

26 Pamenepo ndinadzuka n’kuyang’ana uku ndi uku. Tulo tanga tinali
tokoma.

27 “Masiku akubwera,” akutero Yehova, “pamene ndidzachulukitsa
anthu pamodzi ndi ziweto m’dziko la Israeli ndi la Yuda. 28 Monga
momwe ndinasamalira powazula, powagwetsa, powagumula, powa-
wononga ndi powachita zoyipa, momwemonso ndidzasamala powamanga
ndi powadzala” akutero Yehova. 29 “M’masiku amenewo anthu sadzane-
nanso kuti,

“Makolo adya mphesa zosapsa,
koma mano a ana ndiye achita dziru.

30 M’malo wake, munthu aliyense adzafa chifukwa cha tchimo lake. Iye
amene adzadye mphesa zosapsazo ndiye amene mano ake adzachite
dziru.”

31 “Masiku akubwera,” akutero Yehova,
“pamene ndidzachita pangano latsopano
ndi Aisraeli
ndiponso nyumba ya Yuda.
32 Silidzakhala ngati pangano
limene ndinachita ndi makolo awo
pamene ndinawagwira padzanja
n’kuwatulutsa ku Igupto;
chifukwa anaphwanya pangano langa,
ngakhale ndinali mwamuna wawo,”
akutero Yehova.
33 “Ili ndi pangano limene ndidzachita ndi Aisraeli
atapita masiku amenewo,” akutero Yehova.
“Ndidzayika lamulo langa m’mitima mwawo
ndi kulilemba m’maganizo mwawo.
Ine ndidzakhala Mulungu wawo
ndipo iwo adzakhala anthu anga.
34 Sipadzafunikanso kuti wina aphunzitse mnzake,
kapena munthu wina kuphunzitsa m’bale wake, kunena kuti,
‘Mudziwe Yehova,’
chifukwa onse adzandidziwa Ine,
kuyambira wamng’ono mpaka wamkulu,”
akutero Yehova.
“Ndidzawakhululukira zoyipa zawo
ndipo sindidzakumbukiranso machimo awo.”

35 Yehova akuti,
Iye amene amakhazikitsa dzuwa
kuti liziwala masana,
amene amalamula kuti mwezi ndi nyenyezi
ziziwala usiku,
amene amavundula nyanja
kuti mafunde akokome,
dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse:

36 Ngati zimenezi zilekeka pamaso panga, akutero Yehova, pamenepo
padzakhala pamathero a fuko la Israeli pamaso panga.

37 Yehova akuti,
"Ndidzataya fuko la Israeli chifukwa cha machimo awo.
Ngati patapezeka munthu
amene angathe kupima zakuthambo
n'kufufuza maziko a dziko lapansi."

38 "Taonani masiku akubwera," akutero Yehova, "pamene mzinda wa
Yehova udzamangidwanso kuyambira ku Nsanja ya Hananeli mpaka ku
Chipata cha Ngodya. 39 Malire ake adzayambira pamenepo kupita ku phiri
la Garebu, n'kudzakhota kuloza ku Gowa. 40 Chigwa chonse m'mene
amatayiramo mitembo ndi phulusa, ndiponso minda yonse kuyambira ku Chigwa cha Kidroni mpaka ku ngodya ya Chipata cha Akavalo mbali ya kummawa, adzakhala malo opatulika a Yehova. Mzindawu sadzawuzulanso kapena kuwuwononga."

# 32

*Yeremiya Agula Munda*

1 Yehova anayankhula ndi Yeremiya m'chaka chakhumi cha Zedekiya mfumu ya Yuda, chimene chinalinso chaka cha 18 cha ulamuliro wa
Nebukadinezara. 2 Pa nthawi imeneyi n'kuti ankhondo a mfumu
ya ku Babuloni atazinga Yerusalemu, ndipo mneneri Yeremiya ndiye anamutsekera m'bwalo la alonda m'nyumba yaufumu ya ku Yuda.

3 Tsono Zedekiya mfumu ya Yuda n'kuti itamutsekera m'menemo,
ndipo inati, "N'chifukwa chiyani ukulosera motero? Iwe ukunena kuti,
'Yehova akuti: Ndidzapereka mzinda uno kwa mfumu ya ku Babuloni,
ndipo idzawulanda. 4 Zedekiya mfumu ya Yuda sidzapulumuka m'manja
mwa Ababuloni, koma idzaperekedwa kwa mfumu ya ku Babuloni.
Adzayankhula naye ndi kuonana naye maso ndi maso. 5 Zedekiya
adzatengedwa kupita naye ku Babuloni, kumene adzakhale mpaka ndita-mukhawulitsa, akutero Yehova. Ngakhale iye adzamenyane ndi Babuloni, koma sadzapambana.' "

6 Yeremiya anati, "Yehova wandiwuza kuti: 7 Taonani, Hanameli mwana
wa Salumu, amalume ako akubwera ndipo adzakuwuza kuti, 'Gula munda
wanga wa ku Anatoti, chifukwa iwe ndiwe m'bale wanga ndipo ndiwe woyenera kuwuwombola.' "

8 Ndipo monga momwe Yehova ananenera, Hanameli, msuweni wanga anabweradi ku bwalo la alonda ndipo anati, "Gula munda wanga wa ku Anatoti m'dziko la Benjamini. Popeza ndiwe woyenera kuwugula ndi kukhala wako, gula munda umenewu kuti ukhale wako."

"Ine ndinadziwa kuti amenewa anali mawu a Yehova aja; 9 choncho
ndinagula munda wa ku Anatoti kwa Hanameli msuweni wanga, ndipo
ndinamupatsa masekeli asiliva 17. 10 Ndinasayina panganolo ndikulimata
pamaso pa mboni, kenaka ndinayeza ndalama zasilivazo pa sikelo."
11 Pambuyo pake ndinatenga makalata anga a pangano, imodzi yomatidwa
m'mene munali malamulo onse a panganolo ndi ina yosamatidwa.
12 Ndinapereka makalatawo kwa Baruki mwana wa Neriya, mdzukulu wa Maseya pamaso pa Hanameli msuweni wanga, pamaso pa mboni zimene zinasayina panganoli ndiponso pamaso pa Ayuda onse okhala m'bwalo la alonda.

[13] "Ndinamulangiza Baruki pamaso pa onsewo kuti, [14] 'Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti: Tenga makalata awa a um-
boni wapangano, iyi yokhala ndi chizindikiro ndi yopanda chizindikiro,
uwasunge m'mbiya kuti akhale nthawi yayitali. [15] Pakuti Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti: Anthu adzagulanso
nyumba, minda ndi mitengo yamphesa m'dziko lino.' "

[16] Nditamupatsa makalata a panganowa Baruki mwana wa Neriya,
ndinapemphera kwa Yehova:

[17] "Aa, inu Ambuye Yehova, munalenga dziko lakumwamba ndi
dziko lapansi. Munazilenga ndi dzanja lanu lamphamvu ndipo pal-
ibe chokulakani. [18] Mumaonetsa chikondi chanu kwa anthu osaw-
erengeka koma mumalanga ana chifukwa cha machimo a makolo
awo. Inu ndinu Mulungu Wamkulu ndi Wamphamvu. Dzina lanu
ndinu Yehova Wamphamvuzonse. [19] Zolinga zanu ndi zazikulu ndipo
zochita zanu ndi zamphamvu. Maso anu amaona zonse zimene anthu
amachita. Mumapereka mphotho kwa munthu aliyense molingana
ndi makhalidwe ake ndi ntchito zake. [20] Inu munachita zizindikiro
zozizwitsa ku Igupto, ndipo mwakhala mukuzichita mpaka lero, pakati
pa Aisraeli ndiponso pakati pa anthu onse. Choncho mwadzitchukitsa
mpaka lero lino. [21] Munatulutsa Aisraeli m'dziko la Igupto ndi dzanja
lanu lamphamvu pochita zizindikiro zozizwitsa ndi zodabwitsa zimene
zinaopseza adani anu. [22] Munawapatsa dziko lino limene munalonjeza
mwalumbiro kulipereka kwa makolo awo, dziko loyenda mkaka ndi
uchi. [23] Iwo analowa n'kulitenga kukhala lawo, koma sanamvere Inu
kapena kutsatira lamulo lanu; ndipo sanachite zomwe munawalamula.
Choncho inu mwawagwetsera masautso onsewa."

[24] "Onani momwe adani azingira ndi mitumbira yankhondo mzin-
dawu kuti awulande ndipo akuwuthira nkhondo. Chifukwa cha
lupanga, njala ndi mliri. Mzindawu udzaperekedwa kwa Ababuloni
anthu atafowoka ndi nkhondo, njala ndi mliri. Zimene munkanena zija
zachitikadi monga mukuzionera tsopano. [25] Ngakhale mzindawu udza-
perekedwa kwa Ababuloni, komabe Inu Ambuye Yehova, munandiwuza
kuti, 'Gula munda ndi siliva ndipo upereke ndalamazo pali mboni.' "

[26] Tsono Yehova anawuza Yeremiya kuti, [27] "Taonani, Ine ndine Yehova,
Mulungu wa anthu onse. Kodi chilipo chinthu choti Ine n'kundikanika?
[28] N'chifukwa chake ine Yehova ndikuti: Ndidzawupereka mzinda uno
kwa Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni, amene adzawulanda.
[29] Ndipo Ababuloni amene akuwuthira nkhondo mzinda uno adzalowa
ndi kuwutentha; adzatentha ndi kugwetsa nyumba zimene pa denga pake
anthu ankandipsetsa mtima pofukiza lubani kwa Baala ndi popereka
chopereka cha chakumwa kwa milungu ina.

[30] "Aisraeli ndi Ayuda akhala akuchita zoyipa zokhazokha pamaso panga
kuyambira ubwana wawo. Kunena zoona Aisraeli akumandikwiyitsa
ndi ntchito zawo zoyipa, akutero Yehova. [31] Kuyambira tsiku limene
mzindawu unamangidwa mpaka lero, wakhala ukuwutsa mkwiyo wanga
ndi ukali wanga. N'chifukwa chake ndiyenera kuwuchotsa pamaso panga.
[32] Aisraeli ndi Ayuda, anthu a ku Yuda ndi a ku Yerusalemu, mafumu awo,
nduna zawo, ansembe ndi aneneri awo anandikwiyitsa ndi ntchito zawo
zoyipa. [33] Anandifulatira ndipo ngakhale ndinakhala ndikuwaphunzitsa
kawirikawiri, sanamve kapena kuphunzirapo kanthu. [34] Iwo anayika
mafano awo onyansa m'nyumba imene imadziwika ndi dzina langa ndipo

anayipitsa. 35 Anamanga malo opembedzerapo Baala m'Chigwa cha
Hinomu kuti aziperekapo ana awo aamuna ndi aakazi ngati nsembe kwa
Moleki. Ine sindinawalamulire kutero, ndipo sindinaganizepo n'komwe
kuti iwo angachite chinthu chonyansa chotero, ndi kuchimwitsa anthu a
ku Yuda.

36 "Anthu ponena za mzindawu akuti udzaperekedwa kwa mfumu ya
ku Babuloni mwa nkhondo, njala ndi mliri, koma Yehova Mulungu wa
Israeli akuti, 37 Ine ndidzawasonkhanitsadi anthuwa kuchokera ku mayiko
onse kumene ndinawapirikitsira ndili wokwiya ndi waukali kwambiri.
Ndidzabwera nawo ku malo ano ndipo ndidzawalola kukhala mwamten-
dere. 38 Iwo adzakhala anthu anga, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu
wawo. 39 Ndidzawapatsa mtima umodzi ndi khalidwe limodzi kotero
kuti azidzandiopa nthawi zonse ndipo iwo pamodzi ndi zidzukulu zawo
zinthu zidzawayendera bwino. 40 Ndidzachita nawo pangano losatha:
sindidzaleka kuwachitira zabwino, ndipo ndidzawapatsa mtima woti
azidzandiopa, kuti asadzandisiyenso. 41 Ndidzakondwera powachitira
zabwino, ndipo ndidzawakhazikitsa ndithu m'dziko lino ndi mtima wanga
wonse ndi moyo wanga wonse.

42 "Yehova akuti: Monga momwe ndinagwetsera masautso aakulu
onsewa pa anthuwa, momwemonso ndidzawapatsa zinthu zonse zabwino
zimene ndinawalonjeza. 43 Adzagulanso minda m'dziko muno, limene
inu mukuti, 'Ndi dziko losiyidwa, lopanda anthu kapena nyama, pakuti
linaperekedwa kwa Ababuloni.' 44 Adzagula minda ndi ndalama zasiliva,
ndipo achita pangano, ndi kumata pamaso pa mboni. Izi zidzachitika
m'dziko la Benjamini, ku malo ozungulira Yerusalemu, m'mizinda ya
Yuda, m'mizinda ya ku mapiri, m'mizinda ya kuchigwa ndi yakummwera
ku Negevi. Zoona, ndidzabwezera ufulu wawo, akutero Yehova."

# 33

### *Lonjezo la Kubwezeretsedwa*

1 Yeremiya akanali m'ndende m'bwalo la alonda, Yehova anayankhula
nayenso kachiwiri nati: 2 "Yehova amene analenga dziko lapansi,
kuliwumba ndi kulikhazikitsa; amene dzina lake ndi Yehova, akuti,
3 'Unditame mopemba ndipo ndidzakuyankha. Ndidzakuwuza zinsinsi
zazikulu zimene suzidziwa.' 4 Yehova Mulungu wa Israeli akunenapo pa
za nyumba za mu mzinda muno ndiponso pa za nyumba za mafumu a
Yuda. Zidzagwetsedwa, ndipo palibe chifukwa cholimbana ndi mitumbira
ya nkhondo ya Ababuloni. 5 Ababuloni akubwera kudzawuthira nkhondo
mzindawu ndipo nyumba zake zidzadzaza ndi mitembo ya anthu amene
ndidzawapha mokwiya ndi mwaukali. Ndawufulatira mzinda uno
chifukwa cha zoyipa zake zonse.

6 " 'Pambuyo pake mzindawu ndidzawupatsanso moyo ndi kuwuchir-
itsa; ndidzachiritsa anthu anga ndi kuwapatsa chitetezo ndi mtendere
weniweni. 7 Ndidzawakhazikanso Ayuda ndi Aisraeli ku dziko lawo, ndipo
ndidzawabwezera monga mmene analili poyamba. 8 Ndidzawayeretsa
pochotsa zoyipa zonse zimene anandichitira, ndiponso ndidzawakhu-
lulukira machimo onse amene anachita pondiwukira. 9 Mzinda wa
Yerusalemu udzandipatsa chimwemwe, chiyamiko ndi ulemerero. Anthu
a mitundu yonse adzanditamanda akadzamva za zabwino zonse zimene
ndawuchitira mzindawu. Iwo adzachita mantha ndi kunjenjemera

poona madalitso ochuluka ndi mtendere zimene ndapereka kwa mzinda
umenewu.’

10 “Yehova akuti, ‘Inu mumanena za malo ano kuti ndi bwinja,’
malo opandamo anthu kapena nyama. Komatu mizinda ya Yuda ndi
m’misewu ya mu Yerusalemu m’mene tsopano muli zii mudzamvekanso
11 mfuwu wachimwemwe ndi mawu achisangalalo, mawu a mkwatibwi
ndi mkwati. M’nyumba ya Mulungu mudzamvekanso nyimbo za anthu
amene akudzapereka nsembe zothokoza Yehova. Azidzati,

“Yamikani Yehova Wamphamvuzonse,
popeza Iye ndi wabwino;
pakuti chifundo chake n’chamuyaya.”

Pakuti ndidzabwezeretsa zinthu zabwino za dziko lino monga zinalili
poyamba, akutero Yehova.

12 “Yehova Wamphamvuzonse akuti, ‘Malo ano, a chipululu ndi
wopanda anthu kapena nyama, m’mizinda yake yonse mudzakhala msipu
umene abusa adzadyetserako nkhosa zawo. 13 Ku mizinda ya kumapiri,
ya kuchigwa, ya ku Negevi, ya ku dera la Benjamini, ku dziko lozungulira
Yerusalemu, ndi ku mizinda ya Yuda, nkhosa zidzadutsanso pamaso pa
munthu woziwerenga,’ akutero Yehova.

14 “ ‘Taonani masiku akubwera,’ akutero Yehova, ‘pamene ndidzachitadi
zokoma zimene ndinalonjeza Aisraeli ndi nyumba ya Yuda.

15 “ ‘M’masiku amenewo ndi pa nthawi imeneyo
ndidzaphukitsa Nthambi yolungama kuchokera ku banja la Davide;
munthuyo adzachita zolungama ndi zabwino m’dziko.

16 M’masiku amenewo Yuda adzapulumuka
ndipo Yerusalemu adzakhala mwamtendere.
Dzina limene mzindawu udzadziwike nalo ndi ili:
Yehova Chilungamo Chathu.’

17 Yehova akunena kuti, ‘Davide sadzasowa mdzukulu wolowa m’malo
mwake pa mpando waufumu wa Israeli, 18 ngakhale ansembe, amene
ndi Alevi, sadzasowanso munthu woyima pamaso panga nthawi zonse
wopereka nsembe zopsereza, nsembe zaufa ndi nsembe zina.’ ”

19 Yehova anawuza Yeremiya kuti: 20 Mawu anga ndi awa. Ine
ndinachita pangano ndi usana ndi usiku kuti zizibwera pa nthawi yake.
Pangano limeneli inu simungaliphwanye. 21 Ndinachitanso pangano ndi
Davide, mtumiki wanga kuti nthawi zonse adzakhala ndi mdzukulu
wodzakhala pa mpando wake waufumu. Ndinachitanso pangano ndi
Alevi kuti iwonso adzanditumikira nthawi zonse. Mapangano amenewa
sadzaphwanyidwa nthawi zonse. 22 Ndidzachulukitsa ngati nyenyezi zam-
lengalenga ndiponso ngati mchenga wa m’mbali mwa nyanja zidzukulu za
mtumiki wanga Davide ndiponso za Alevi amene amanditumikira Ine.

23 Yehova anafunsa Yeremiya kuti, 24 “Kodi sunamve mmene anthu
ena akumanenera kuti, ‘Yehova wakana maufumu awiriwa amene
Iye anawasankha.’ Kotero anthuwo akunyoza anthu anga ndipo
sakuwayesanso mtundu wa anthu. 25 ‘Koma Ine Yehova ndinachita
pangano ndi usana ndi usiku. Ndinakhazikitsanso malamulo oyendetsa
dziko lakumwamba ndi dziko lapansi, 26 monga ndachita zimenezi mot-
simikiza, choncho ndidzasunga pangano limene ndinachita ndi zidzukulu
za Yakobo ndi Davide mtumiki wanga. Ndidzasankha mmodzi mwa ana a
Davide kuti alamulire zidzukulu za Abrahamu, Isake ndi Yakobo. Komatu
ndidzawamvera chifundo ndi kuwakhazikanso pabwino.’ ”

# 34

### *Chenjezo kwa Zedekiya*

1 Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni ndi gulu lake lonse lankhondo,
pamodzi ndi maufumu onse a pa dziko lapansi amene ankawalamulira
ndiponso anthu a mitundu yonse ankathira nkhondo Yerusalemu ndi
mizinda yonse yozungulira Yehova anayankhula ndi Yeremiya kuti,
2 "Yehova, Mulungu wa Israeli akuti: Pita kwa Zedekiya mfumu ya
Yuda ndipo ukamuwuze kuti Yehova akuti mzinda uno ndidzawupereka
m'manja mwa mfumu ya ku Babuloni ndipo adzawutentha ndi moto.
3 Iweyo sudzapulumuka m'manja mwake koma udzagwidwa ndithu ndipo
adzakupereka m'manja mwake. Udzayiona mfumu ya ku Babuloni maso
ndi maso ako ndipo udzayankhula nayo pakamwa ndi pakamwa. Ndipo
udzapita ku Babuloni.

4 "Koma iwe Zedekiya mfumu ya Yuda, imva lonjezo ili la Yehova. Izi
ndi zimene Yehova akunena za iwe: Sudzaphedwa pa nkhondo; 5 udzafera
pa mtendere. Monga anthu ankafukiza lubani poyika maliro a makolo
ako akale, amene anali mafumu iwe usanalowe ufumu, choncho nawenso
podzayika maliro ako adzafukiza lubani ndipo polira azidzati, 'Kalanga,
mbuye wanga!' Ine mwini ndalonjeza zimenezi, akutero Yehova."

6 Ndipo mneneri Yeremiya anawuza zonsezi Zedekiya mfumu ya Yuda,
mu Yerusalemu. 7 Nthawi imeneyi n'kuti gulu lankhondo la mfumu ya ku
Babuloni likuthira nkhondo Yerusalemu ndi mizinda ina yotsala ya Yuda,
Lakisi ndi Azeka. Imeneyi yokha ndiye inali mizinda yotetezedwa yotsala
ya ku Yuda.

### *Kumasulidwa kwa Akapolo*

8 Yehova anayankhulanso ndi Yeremiya. Nthawi imeneyi n'kuti mfumu
Zedekiya atachita pangano ndi anthu onse a mu Yerusalemu kuti alengeze
zakuti akapolo awo adzawamasule. 9 Aliyense amene anali ndi akapolo
a Chihebri, aamuna kapena aakazi awamasule; palibe amene ayenera
kusunga mu ukapolo Myuda mnzake. 10 Choncho akuluakulu pamodzi
ndi anthu onse amene anachita pangano ili anagwirizana kuti amasule
akapolo awo aamuna ndi aakazi ndi kuti asawasungenso mu ukapolo.
Iwo anachitadi zimenezi ndipo anawamasuladi. 11 Koma pambuyo pake
anasintha maganizo awo ndi kuwatenganso amuna ndi akazi amene
anawamasula aja ndipo anawasandutsanso akapolo.

12 Tsono Yehova anawuza Yeremiya kuti: 13 "Yehova Mulungu wa Israeli
akuti: Ine ndinachita pangano ndi makolo anu pamene ndinawatulutsa ku
Igupto, m'dziko la ukapolo. Ine ndinati, 14 'Chaka chachisanu ndi chiwiri
chilichonse aliyense wa inu ayenera kumasula m'bale wake wa Chihebri
amene anadzigulitsa yekha kwa inuyo. Iyeyo amasulidwe akagwira
ntchito zaka zisanu ndi chimodzi, mumulole apite mwaufulu.' Komatu
makolo anu sanandimvere kapena kusamala konse. 15 Posachedwa
pomwepa inu munalapa ndi kuchita zinthu zabwino pamaso panga:
Aliyense wa inu anamasula m'bale wake. Ndipo munachita pangano
pamaso panga m'Nyumba imene imadziwika ndi dzina langa kuti mudza-
chitadi zimenezi. 16 Koma tsopano mwasintha maganizo anu ndipo
mwayipitsa dzina langa. Mwatenganso ukapolo aamuna ndi aakazi amene
munawamasula aja kuti apite kumene akufuna. Mwawakakamiza kuti
akhalebe akapolo anu.

17 “N’chifukwa chake Yehova akuti: Inu simunandimvere Ine; simu-
nalengeze kuti abale anu amasulidwe. Chabwino! Ine ndidzakupatsani
ufulu; ufulu wake ukhala wophedwa ndi nkhondo, mliri ndi njala.
Ndidzakusandutsani chinthu chochititsa mantha pakati pa maufumu onse
a dziko lapansi. 18 Inu simunasunge pangano limene munachita ndi
Ine. Simunasamale lonjezo limene munachita pamaso panga. Choncho
ndidzakusandutsani ngati mwana wang’ombe uja amene ankamudula
pawiri napita pakati pa zigawozo. 19 Amene ankadutsa pakati pa zigawozo
anali atsogoleri a Yuda ndi Yerusalemu, akuluakulu a bwalo, ansembe
ndi anthu onse a m’dzikomo. 20 Onsewa ndidzawapereka kwa adani
awo amene akufuna kuwapha. Mitembo yawo idzakhala chakudya cha
mbalame zamlengalenga ndi zirombo za dziko lapansi.

21 “Ndidzapereka Zedekiya mfumu ya Yuda ndi nduna zake kwa adani
awo amene akufuna kuwapha, kwa gulu lankhondo la mfumu ya ku
Babuloni limene nthawi ino layamba kubwerera m’mbuyo. 22 Taonani, Ine
ndidzawalamula, akutero Yehova, ndipo ndidzawabweretsanso ku mzinda
uno. Adzathira nkhondo mzindawu, kuwulanda ndi kuwutentha. Ndipo
Ine ndidzasandutsa chipululu mizinda ya Yuda kotero kuti palibe amene
adzakhalemo.”

# 35

*Arekabu*

1 Yehova anayankhula ndi Yeremiya nthawi ya ulamuliro wa Yehoy-
akimu mwana wa Yosiya mfumu ya Yuda, kuti: 2 “Pita ku banja la Arekabu
ndipo ukawayitane kuti abwere m’chipinda chimodzi cha Nyumba ya
Yehova ndipo akafika uwapatse vinyo kuti amwe.”

3 Choncho ndinakatenga Yaazaniya (mwana wa Yeremiya winanso
amene anali mwana wa Habaziniya), abale ake, ana ake onse aamuna ndi
banja lonse la Arekabu. 4 Ndinabwera nawo ku Nyumba ya Yehova, ku
chipinda cha ophunzira a mneneri Hanani mwana wa Igidaliya, munthu
wa Mulungu. Chipinda chimenechi chinali pafupi ndi chipinda cha
akuluakulu, chimene chinali pamwamba pa chipinda cha Maaseya mwana
wa Salumu, mlonda wa pa khomo. 5 Kenaka ndinayika mabotolo odzaza
ndi vinyo ndi zikho zake pamaso pa Arekabu ndipo ndinawawuza kuti,
“Imwani vinyoyu.”

6 Koma iwo anayankha kuti, “Ife sitimwa vinyo, chifukwa kholo
lathu Yehonadabu mwana wa Rekabu anatilamula kuti, ‘Inuyo ngakhale
zidzukulu zanu, musadzamwe vinyo mpaka kalekale. 7 Musadzamange
nyumba kapena kufesa mbewu, kapena kulima minda ya mpesa; mu-
sadzakhale ndi zinthu zimenezi. M’malo mwake muzidzakhale m’matenti.
Mukadzatero mudzakhala nthawi yayitali m’dziko limene mukukhalamo.’
8 Ife takhala tikumvera zonse zimene kholo lathu Yehonadabu mwana
wa Rekabu anatilamula. Ife ngakhale akazi athu kapena ana athu
aamuna ndi aakazi sitinamwepo vinyo 9 kapena kumanga nyumba kuti
tizikhalamo kapenanso kukhala ndi minda ya mpesa, minda ina iliyonse
kapena mbewu. 10 Koma takhala m’matenti ndipo tamvera kwathunthu
chilichonse chimene kholo lathu Yehonadabu anatilamula. 11 Koma
pamene Nebukadinezara mfumu ya Babuloni anathira nkhondo dziko
lino, ife tinati, ‘Tiyeni tichoke, tipite ku Yerusalemu kuti tithawe magulu
ankhondo a Akasidi ndi Aaramu.’ Kotero ife takhala tikukhala mu
Yerusalemu.”

12 Yehova anayankhulanso ndi Yeremiya kuti, 13 "Iyeyu, Yehova Mulungu
wa Israeli anawuza Yeremiya kuti: Pita ukawawuze anthu a ku Yuda ndi a
ku Yerusalemu kuti, 'Kodi simungatengeko phunziro ndi kumvera mawu
anga?' akutero Yehova. 14 'Yehonadabu mwana wa Rekabu analamula
ana ake kuti asamwe vinyo ndipo lamulo limeneli alisunga. Mpaka lero
lino iwo samwa vinyo, chifukwa akumvera lamulo la kholo lawo. Koma
Ine ndakhala ndikuyankhula nanu kawirikawiri kukuchenjezani, koma
inu simunandimvere Ine. 15 Kawirikawiri ndakhala ndikutumiza atumiki
anga, aneneri, kwa inu. Iwo akhala akukuwuzani kuti, 'Aliyense wa
inu asiye ntchito zake zoyipa ndi kukonza makhalidwe ake; musatsatire
milungu ina ndi kumayitumikira. Pamenepo mudzakhala m'dziko limene
ndinakupatsani ndi makolo anu.' Komabe inu simunasamale zimenezi
kapena kundimvera Ine. 16 Zidzukulu za Yehonadabu mwana wa Rekabu
zakhala zikumvera lamulo limene kholo lawo anazilamula, koma inuyo
simunandimvere Ine.
17 "N'chifukwa chake Yehova Mulungu Wamphamvuzonse, Mulungu
wa Israeli akuti, 'Ndidzagwetsera pa Yuda ndi pa onse okhala mu
Yerusalemu masautso onse amene ndinakonza chifukwa sanandimvere.
Ndinawayitana koma iwo sanayankhe.' "
18 Yeremiya anawuza banja la Arekabu mawu onse a Yehova
Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli, kuti, "Munamvera lamulo la
kholo lanu Yehonadabu ndipo mwatsatira malangizo ake onse ndi kuchita
chilichonse chimene anakulamulani." 19 Tsono Yehova Wamphamvu-
zonse, Mulungu wa Israeli akuti, "Yehonadabu mwana wa Rekabu
sadzasowa munthu wonditumikira Ine nthawi zonse."

# 36

*Yehoyakimu Atentha Buku la Yeremiya*

1 Chaka chachinayi cha Yehoyakimu mwana wa Yosiya mfumu ya Yuda,
Yehova anayankhula ndi Yeremiya kuti, 2 "Tenga buku ndipo ulembemo
mawu onse amene ndayankhula nawe otsutsa Israeli, Yuda ndi mitundu
yonse ya anthu, kuyambira nthawi imene ndinayamba kuyankhula nawe
pa nthawi ya ulamuliro wa Yosiya mpaka lero lino. 3 Mwina mwake anthu
a ku Yuda adzamva za zoopsa zonse zimene ndakonza kuti ndiwachitire,
ndipo munthu aliyense adzatembenuka ndi kusiya ntchito zake zoyipa.
Motero ndidzawakhululukira zoyipa zawo ndi machimo awo."
4 Tsono Yeremiya anayitana Baruki mwana wa Neriya. Baruki analemba
m'buku mawu onse amene Yeremiya ankamuwuza, mawu amene Yehova
anamuwuza Yeremiya. 5 Kenaka Yeremiya anawuza Baruki kuti, "Ine
andiletsa kupita ku Nyumba ya Mulungu. 6 Tsono iwe upite ku Nyumba ya
Yehova pa tsiku losala kudya ndipo ukawerenge mawu a Yehova ochokera
m'bukumu amene ndinakulembetsa anthu onse akumva. Ukawaweren-
gere anthu onse a ku Yuda amene amabwera ku Nyumba ya Mulungu
kuchokera ku mizinda yawo. 7 Mwina mwake adzapempha kwa Yehova
ndipo aliyense adzatembenuka ndi kusiya makhalidwe ake oyipa pakuti
mkwiyo ndi ukali wa Yehova pa anthu awa ndi woopsa kwambiri."
8 Baruki mwana wa Neriya anachita zonse zimene mneneri Yeremiya
anamuwuza kuti achite. M'nyumba ya Yehova, iye anawerenga mawu a
Yehova ochokera m'bukulo. 9 Pa mwezi wachisanu ndi chinayi wa chaka
chachisanu cha Yehoyakimu mwana wa Yosiya mfumu ya Yuda, anthu
onse a mu Yerusalemu ndi onse amene anabwera kumeneko kuchokera
ku mizinda ya Yuda, anapangana za kusala kudya kuti apepese Yehova.

10 Atayima pa chipinda cha Gemariya mwana wa mlembi Safani, chimene
chinali m'bwalo lapamwamba, pafupi ndi Chipata Chatsopano cholowera
ku Nyumba ya Yehova, Baruki anawerenga mawu onse a Yeremiya amene
anali m'buku muja kwa anthu onse amene anali ku Nyumba ya Yehova.
11 Mikaya mwana wa Gemariya, mwana wa Safani, atamva mawu
onse a Yehova ochokera m'bukumo, 12 anapita ku nyumba ya mfumu
nakalowa ku chipinda cha mlembi. Akuluakulu, mlembi Elisama, Delaya
mwana wa Semaya, Elinatani mwana wa Akibori, Gemariya mwana
wa Safani, Zedekiya mwana wa Hananiya pamodzi ndi akuluakulu ena
onse, anali atasonkhana kumeneko. 13 Tsono Mikaya anawafotokozera
mawu onse amene anamva pamene Baruki ankawerenga buku lija anthu
onse akumva. 14 Pambuyo pake akuluakulu onsewo anatuma Yehudi
mwana wa Netaniya, mwana wa Selemiya, mwana wa Kusi, kwa Baruki
kukamuwuza kuti, "Bwera ndi buku limene unawerenga kwa anthu."
Ndipo Baruki mwana wa Neriya anapita nalo bukulo kwa anthuwo. 15 Iwo
anati, "Khala pansi, ndipo tiwerengere bukuli."
Ndipo Baruki anawawerengera. 16 Atamva mawu onsewo,
anayang'anana mwa mantha ndipo anamuwuza Baruki kuti, "Ndithudi
tikafotokozera mfumu mawu onsewa." 17 Tsono anamufunsa Baruki
kuti, "Tatiwuze, unalemba bwanji mawu onsewa? Kodi ndi Yeremiya
anakulembetsa zimenezi?"
18 Baruki anayankha kuti, "Inde, ndi Yeremiya amene anandiwuza
mawu onsewa, ndipo ine ndinawalemba ndi utoto m'bukumu."
19 Kenaka akuluakuluwo anamuwuza Baruki kuti, "Iweyo ndi Yeremiya,
pitani mukabisale. Munthu aliyense asadziwe kumene muli."
20 Atayika bukulo m'chipinda cha mlembi Elisama, analowa m'bwalo,
napita kwa mfumu ndi kukayifotokozera zonse. 21 Itamva zimenezi
mfumu inatuma Yehudi kuti akatenge bukulo, ndipo Yehudi anakalitenga
ku chipinda cha mlembi Elisama ndipo anawerengera mfumu pamodzi
ndi akuluakulu ake amene anali naye. 22 Unali mwezi wachisanu ndi
chinayi ndipo mfumu inali m'nyumba ya pa nyengo yozizira, ikuwotha
moto umene anasonkha. 23 Yehudi ankati akawerenga masamba atatu
kapena anayi a bukulo, mfumu inkawang'amba ndi mpeni ndi kuwaponya
pa moto ndipo anapitiriza kuchita zimenezi mpaka buku lonse linapsa.
24 Mfumu pamodzi ndi omutumikira ake onse amene anamva mawu
onsewa sanachite mantha kapena kung'amba zovala zawo. 25 Ngakhale
kuti Elinatani, Delaya, ndi Gemariya anapempha mfumu kuti isatenthe
bukulo, mfumuyo sinawamvere. 26 M'malo mwake, mfumu inalamula
Yerahimeeli mwana wake, Seraya mwana wa Azirieli ndi Selemiya mwana
wa Abideeli kuti agwire mlembi Baruki ndi mneneri Yeremiya. Koma
pamenepo n'kuti Yehova atawabisa.
27 Mfumu itatentha buku limene linali ndi mawu amene Yeremiya ana-
mulembetsa Baruki, Yehova anayankhula ndi Yeremiya kuti, 28 "Tenganso
buku lina ndipo ulembe mawu onse amene anali m'buku loyamba lija,
limene Yehoyakimu analitentha. 29 Ndiponso akamuwuze Yehoyakimu
mfumu ya Yuda kuti, 'Yehova akuti: Iwe unatentha buku lija ndipo unati:
N'chifukwa chiyani unalemba kuti mfumu ya ku Babuloni idzabwera
ndithu kudzawononga dziko lino ndi kupha anthu pamodzi ndi nyama
zomwe?' 30 N'chifukwa chake kunena za Yehoyakimu mfumu ya Yuda
Yehova akuti sipadzaoneka munthu wina wolowa m'malo mwake pa
mpando wa Davide. Akadzafa mtembo wake udzaponyedwa kunja

ndipo udzakhala pa dzuwa masana, ndi pachisanu chowundana usiku.
31 Ndidzamulanga pamodzi ndi ana ake ndiponso omutumikira ake
chifukwa cha zoyipa zawo; ndidzagwetsa pa iwo ndi pa onse amene
akukhala mu Yerusalemu ndiponso pa anthu a ku Yuda masautso onse
amene ndinawanena, chifukwa sanamvere."
32 Choncho Yeremiya anatenga buku lina napatsa mlembi Baruki
mwana wa Neriya, ndipo Yeremiya anamulembetsa mawu onse amene
anali m'buku limene Yehoyakimu mfumu ya Yuda anatentha. Ndipo
anawonjezerapo mawu ambiri monga omwewo.

# 37

*Atsekera Yeremiya M'ndende*

1 Nebukadinezara mfumu ya Babuloni, inakhazika pa mpando waufumu
Zedekiya mwana wa Yosiya kukhala mfumu ya Yuda. Iye analowa
m'malo mwa Yehoyakini mwana wa Yehoyakimu. 2 Koma Zedekiya
kapena atumiki ake ngakhalenso anthu a m'dzikomo sanasamalire mawu
a Yehova amene anayankhula kudzera mwa mneneri Yeremiya.
3 Tsono Zedekiya anatuma Yehukali mwana wa Selemiya ndi wansembe
Zefaniya mwana wa Maseya kwa mneneri Yeremiya ndi uthenga uwu:
"Chonde tipempherereni kwa Yehova Mulungu wathu."
4 Nthawi imeneyinso n'kuti Yeremiya ali ndi ufulu woyenda pakati pa
anthu chifukwa anali asanaponyedwe m'ndende. 5 Nthawi imeneyinso
n'kuti gulu lankhondo la Farao litatuluka m'dziko la Igupto. Ndipo
Ababuloni amene anali atazinga Yerusalemu atamva zimenezi, anachoka
ku Yerusalemuko.
6 Tsono Yehova anawuza mneneri Yeremiya kuti, 7 "Uyiwuze mfumu ya
Yuda imene inakutuma kuti udzapemphe nzeru kwa ine kuti Ine Yehova,
Mulungu wa Israeli ndikuti, gulu lankhondo la Farao limene linatuluka
kuti lidzakuthandize lidzabwerera kwawo ku Igupto. 8 Ndipo Ababuloni
adzabwerera kudzathira nkhondo mzinda uno. Iwo adzawugonjetsa ndi
kuwutentha.
9 "Yehova akuti: Musadzinyenge, n'kumaganiza kuti, 'Ndithu Ababuloni
adzatisiya.' Ndithudi sadzakusiyani! 10 Ngakhale mutagonjetsa gulu lonse
lankhondo la Ababuloni limene likukuthirani nkhondo ndipo m'matenti
mwawo ndikutsala anthu ovulala okhaokha, amenewo adzabwera ndi
kudzatentha mzinda uno."
11 Gulu lankhondo la Ababuloni litaleka kuthira nkhondo mzinda
wa Yerusalemu chifukwa choopa gulu lankhondo la Farao, 12 Yeremiya
ananyamuka kuchoka ku Yerusalemu ndi kumapita ku dziko la Benjamini
kuti akalandire gawo lake la minda ya makolo ake. 13 Koma atafika
pa Chipata cha Benjamini, mkulu wa alonda amene dzina lake linali
Iriya mwana wa Selemiya, mwana wa Hananiya, anagwira mneneri
Yeremiyayo ndipo anati, "Iwe ukuthawira kwa Ababuloni!"
14 Yeremiya anati, "Zimenezo si zoona! Ine sindikuthawira kwa Abab-
uloni." Koma Iriya sanamumvere. M'malo mwake anagwira Yeremiya
n'kupita naye kwa akuluakulu. 15 Akuluakuluwo anamupsera mtima
Yeremiya ndipo anamukwapula ndi kumuyika m'nyumba ya mlembi
Yonatani, imene anayisandutsa ndende.
16 Yeremiya anayikidwa m'ndende ya pansi pa nthaka, kumene anakha-
lako nthawi yayitali. 17 Kenaka Mfumu Zedekiya inatuma anthu kuti
akayitane Yeremiya ndipo anabwera naye ku nyumba ya mfumu. Atafika

mfumu inamufunsa mwamseri kuti, “Kodi pali mawu ena amene Yehova wakuwuza?”

Yeremiya anayankha kuti, “Inde. Inu mfumu mudzaperekedwa kwa mfumu ya ku Babuloni.”

18 Pamenepo Yeremiya anafunsa Mfumu Zedekiya kuti, “Kodi ndakulak-
wirani chiyani inuyo kapena akuluakulu anu kapenanso anthu awa, kuti
mundiyike m’ndende? 19 Kodi ali kuti aneneri anu amene anakuloserani
kuti, ‘Mfumu ya ku Babuloni sidzakuthirani nkhondo pamodzi ndi dziko
lino’? 20 Koma tsopano, mbuye wanga mfumu, chonde tamverani. Loleni
ndinene pempho langa pamaso panu: Musandibwezere ku nyumba ya
mlembi Yonatani, kuopa kuti ndingakafere kumeneko.”

21 Tsono Mfumu Zedekiya analamula kuti Yeremiya asungidwe m’bwalo
la alonda. Ankamupatsa buledi tsiku ndi tsiku amene ankamugula
kwa ophika buledi. Anapitiriza kutero mpaka buledi yense anatha mu
mzindamo. Choncho Yeremiya anapitirira kukhala m’bwalo la alonda.

# 38

*Yeremiya Aponyedwa M’chitsime cha Matope*

1 Sefatiya mwana wa Matani, Gedaliya mwana wa Pasi-Huri, Yukali
mwana wa Selemiya, ndi Pasi-Huri mwana wa Malikiya anamva zimene
Yeremiya ankawuza anthu onse kuti, 2 “Yehova akuti, ‘Aliyense amene
akhale mu mzinda muno adzafa ndi nkhondo njala kapena mliri. Koma
aliyense amene atatuluke kukadzipereka kwa Ababuloni adzapulumutsa
moyo wake; iyeyo adzakhala ndi moyo. 3 Mzinda uno udzaperekedwa
ndithu kwa gulu lankhondo la mfumu ya ku Babuloni, amene adzawu-
lande.’ ”

4 Tsono akuluakuluwo anawuza mfumu kuti, “Munthu uyu ayenera kuphedwa. Iye akutayitsa mtima asilikali pamodzi ndi anthu onse amene atsala mu mzinda muno, chifukwa cha zimene akuwawuza. Munthu ameneyu sakufunira zabwino anthuwa koma chiwonongeko chawo.”

5 Mfumu Zedekiya anayankha kuti, “Munthuyu ali m’manja mwanu. Ine sindingakuletseni chimene mukufuna kumuchitira.”

6 Choncho iwo anatenga Yeremiya nakamuponya m’chitsime cha Malikiya, mwana wa mfumu, chimene chinali m’bwalo la alonda. Iwo anamutsitsira m’dzenjemo ndi chingwe. Munalibe madzi koma matope okhaokha, ndipo Yeremiya anamira m’matopewo.

7 Koma Ebedi-Meleki, Mkusi, mmodzi mwa anthu ofulidwa ogwira
ntchito m’nyumba ya mfumu, anamva kuti Yeremiya anamuponya
m’chitsime. Nthawi imeneyo n’kuti mfumu ili ku chipata cha Ben-
jamini. 8 Ebedi-Meleki anatuluka ku nyumba ya mfumu kukayiwuza kuti,
9 “Mbuye wanga mfumu, zimene anthu awa amuchitira mneneri Yeremiya
ndi zoyipa kwambiri. Iwo amuponya m’chitsime, ndipo adzafa ndi njala
chifukwa buledi watha mu mzinda muno.”

10 Tsono mfumu inalamula Ebedi-Meleki, Mkusi, kuti, “Tenga anthu makumi atatu, ndipo mukamutulutse m’chitsimemo mneneri Yeremiya asanafe.”

11 Pamenepo Ebedi-Meleki anatenga anthuwo, napita nawo ku nyumba
ya mfumu ya pansi pa chipinda chosungiramo chuma. Kumeneko
anakatengako sanza ndipo anatsitsira sanzazo ndi chingwe m’chitsime
m’mene munali Yeremiya. 12 Ebedi-Meleki, Mkusi, anawuza Yeremiya

kuti, "Ika sanzazo mkwapa mwako kuti zingwe zingakupweteke."
Yeremiya anachitadi zimenezi, 13 ndipo anamukoka ndi zingwe ndi
kumutulutsa m'chitsimecho. Ndipo Yeremiya anakhalabe ku bwalo la alonda.

### *Zedekiya Afunsanso Yeremiya*

14 Tsiku lina Mfumu Zedekiya anayitana mneneri Yeremiya ndipo anabwera naye ku chipata chachitatu cha Nyumba ya Yehova. Mfumu inawuza Yeremiya kuti, "Ndikufuna kukufunsa kanthu kena, ndipo usandibisire chilichonse."

15 Yeremiya anati kwa Zedekiya, "Ndikakuyankhani, kodi simundipha? Ngakhaletu ine nditakulangizani, inu simudzandimvera."

16 Koma Mfumu Zedekiya mwachinsinsi inalumbira kwa Yeremiya kuti, "Pali Yehova wamoyo, amene amatipatsa moyo, sindidzakupha ngakhalenso kukupereka kwa amene akufuna kukuphawa."

17 Pamenepo Yeremiya anati kwa Zedekiya, "Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti, 'Ngati mutuluka kukadzipereka kwa ankhondo a mfumu ya ku Babuloni, mudzakhala ndi moyo ndipo mzinda uno sadza-
wutentha, inu pamodzi ndi banja lanu mudzakhala ndi moyo. 18 Koma
ngati simutuluka kukadzipereka kwa ankhondo a mfumu ya ku Babuloni, mzinda uno udzaperekedwa kwa Ababuloni ndipo adzawutentha; inuyo simudzapulumuka m'dzanja mwawo.' "

19 Mfumu Zedekiya inati kwa Yeremiya, "Ine ndikuopa Ayuda amene anathawira kale kwa Ababuloni, pakuti mwina Ababuloniwo adzandipereka kwa Ayudawo ndipo iwowo adzandizunza."

20 Yeremiya anayankha kuti, "Ngati mumvera Yehova ndi kuchita zimene ndakuwuzani, ndiye kuti zinthu zidzakuyenderani bwino. Inu
simudzaphedwa. 21 Koma mukakana kudzipereka, chimene Yehova
wandiwululira ndi ichi: 22 Akazi onse amene atsala m'nyumba ya mfumu
ya Yuda adzaperekedwa kwa akuluakulu a mfumu ya ku Babuloni. Akazi amenewo adzakuwuzani kuti,

" 'Abwenzi ako okhulupirika aja anakusokeretsa,
ndipo anakugonjetsa.
Poti tsopano miyendo yako yazama m'matope;
abwenzi ako aja akusiya.'

23 "Akazi pamodzi ndi ana anu adzaperekedwa kwa Ababuloni. Inuyo simudzapulumuka m'manja mwawo koma mfumu ya ku Babuloni idzakugwirani; mzinda uno adzawutentha."

24 Pamenepo Zedekiya anati kwa Yeremiya, "Usawuze munthu wina
aliyense zimene takambiranazi, ukatero udzaphedwa. 25 Akuluakulu
akamva kuti ndinayankhula nawe ndipo akabwera kwa iwe n'kudzakufunsa kuti, 'Tiwuze zimene unanena kwa mfumu ndi zimene
mfumu inanena kwa iwe; usatibisire, ukatero tidzakupha,' 26 udzawawuze
kuti, 'Ine ndimapempha mfumu kuti isandibwezerenso ku nyumba ya Yonatani kuti ndikafere kumeneko.' "

27 Akuluakulu onse anabweradi kwa Yeremiya kudzamufunsa. Iye anawayankha monga momwe mfumu inamulamula. Choncho palibe amene ananenanso kanthu, pakuti palibe amene anamva zomwe anakambirana ndi mfumu.

28 Ndipo Yeremiya anakhalabe m'bwalo la alonda mpaka tsiku limene mzinda wa Yerusalemu unalandidwa.

# 39

### *Kugonjetsedwa kwa Yerusalemu*

1 Mzinda wa Yerusalemu anawulanda motere: M'chaka chachisanu ndi
chinayi cha Zedekiya mfumu ya Yuda, mwezi wakhumi, Nebukadinezara
mfumu ya ku Babuloni anabwera ndi gulu lake lonse kudzathira nkhondo
mzinda wa Yerusalemu ndipo anawuzinga mzindawo. 2 Ndipo pa tsiku
lachisanu ndi chinayi la mwezi wachinayi wa chaka cha khumi ndi
chimodzi cha Zedekiya, malinga a mzindawo anabowoledwa. 3 Pamenepo
akuluakulu onse a mfumu ya ku Babuloni anabwera nakakhala pa
Chipata Chapakati. Akuluwo ndi awa: Nerigali-Sarezeri, Samugara Nebo,
Sarisekimu mkulu wa nduna, Nerigali-Sarezeri winanso mlangizi wa
mfumu ndi akuluakulu onse a mfumu ya ku Babuloni. 4 Zedekiya mfumu
ya Yuda pamodzi ndi ankhondo ake atawaona, anathawa mu mzindawo
usiku podzera ku munda wa mfumu, kudutsa chipata cha pakati pa
makoma awiri. Anathawira ku Araba.
5 Koma gulu la ankhondo la ku Babuloni linalondola ndi kumupeza
Zedekiyayo m'chigwa cha ku Yeriko. Anamugwira napita naye kwa
Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni ku Ribula m'dziko la Hamati
kumene anagamula mlandu wake. 6 Ku Ribulako, mfumu ya ku
Babuloni inapha ana aamuna a Zedekiya iyeyo akuona. Inaphanso anthu
olemekezeka onse a ku Yuda. 7 Kenaka inakolowola maso a Zedekiya ndi
kumumanga ndi maunyolo a mkuwa n'kupita naye ku Babuloni.
8 Ababuloni anatentha nyumba ya mfumu ndi nyumba za anthu,
ndiponso anagwetsa malinga a Yerusalemu. 9 Nebuzaradani, mtsogoleri
wa alonda ankhondo a mfumu, anatenga ukapolo anthu onse otsala mu
mzindamo kupita nawo ku Babuloni, pamodzi ndi amene anadzipereka
kale kwa iye. 10 Koma Nebuzaradani, mtsogoleri wa alonda ankhondo
anasiya m'dziko la Yuda anthu ena osauka, amene analibe chilichonse;
ndipo anawapatsa minda ya mpesa ndi minda inanso.
11 Tsono Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni inatuma mawu kwa
Nebuzaradani mtsogoleri wa alonda ankhondo a mfumu za Yeremiya.
Iye anati: 12 "Mutenge, umusamale bwino, ndipo usamuvute koma umu-
chitire zimene afuna." 13 Choncho Nebuzaradani mtsogoleri wa alonda,
Nebusazibani mkulu wa nduna, Nerigali-Sarezeri mlangizi wamkulu
wa mfumu ndi akuluakulu onse a mfumu ya ku Babuloni 14 anatuma
anthu nakamutulutsa Yeremiya m'bwalo la alonda. Anakamupereka kwa
Gedaliya mwana wa Ahikamu, mwana wa Safani, kuti amutumize ku
nyumba yake. Ndipo Yeremiya anakhala pakati pa abale ake.
15 Yeremiya ali m'ndende ku bwalo la alonda, Yehova anayankhula naye:
16 "Pita ukamuwuze Ebedi-Meleki, Mkusi, kuti, 'Yehova Wamphamvu-
zonse, Mulungu wa Israeli akuti: Zidzachitikadi zimene ndinanena
zokhudza mzinda uno; ndipo zidzakhala zoyipa osati zabwino ayi.
Zimenezi zidzachitika pa nthawi yake iwe ukuona. 17 Koma ndidza-
kupulumutsa pa tsiku limenelo, akutero Yehova; sudzaperekedwa kwa
anthu amene umawaopa. 18 Ndithu ndidzakupulumutsa; sudzaphedwa pa
nkhondo koma udzapulumuka, chifukwa wadalira Ine, akutero Yehova.' "

# 40

### *Amasula Yeremiya*

1 Yehova anayankhula ndi Yeremiya pamene Nebuzaradani mtsogoleri
wa asilikali olonda mfumu anamasula Yeremiyayo ku Rama. Anamupeza
Yeremiya ali womangidwa ndi unyolo pamodzi ndi am'ndende ena onse
a ku Yerusalemu ndi a ku Yuda amene ankapita nawo ku ukapolo ku
Babuloni. 2 Mtsogoleriyu anamupeza Yeremiya, anamuwuza kuti, "Yehova
Mulungu wako analengeza kale zakuti malo ano adzawonongedwa.
3 Ndipo tsopano Yehova wachitadi zimenezi monga mmene ananenera.
Izi zonse zachitika chifukwa anthu inu munachimwira Yehova ndipo
simunamumvere. 4 Koma tsopano taona, lero ndikukumasula unyolo
umene unali m'manja mwako. Ngati ukufuna kupita nane ku Babuloni,
tiye ndipo adzakusamala bwino. Koma ngati sukufuna kupita, ndiye
usapite. Dziko ndi limeneli monga ukulioneramo. Uli ndi ufulu kupita
kulikonse kumene ukufuna." 5 Yeremiya asanayankhe, Nebuzaradani
anamuwuzanso kuti, "Ngati supita ndiye pita, ubwerere kwa Gedaliya,
mwana wa Ahikamu, mdzukulu wa Safani, amene mfumu ya ku Babuloni
inamusankha kuti akhale bwanamkubwa wa Yuda. Ukakhale naye pakati
pa anthu, kapena upite kulikonse ukufuna."

Ndipo mtsogoleri uja anamupatsa Yeremiya chakudya ndi mphatso zina
ndi kumulola kuti apite. 6 Motero Yeremiya anapita kwa Gedaliya mwana
wa Ahikamu ku Mizipa ndipo anakakhala naye kumeneko pakati pa anthu
amene anatsala m'dzikomo.

### *Kuphedwa kwa Gedaliya*

7 Panali atsogoleri ena a nkhondo ndi anthu awo amene sanadzipereke
nawo. Iwowa anamva kuti mfumu ya ku Babuloni inasankha Gedaliya
mwana wa Ahikamu kukhala bwanamkubwa wa dzikolo ndipo kuti
yamuyika kukhala wolamulira amuna, akazi ndi ana amene anali osauka
kwambiri m'dzikomo, amene sanawagwire ukapolo kupita nawo ku
Babuloni. 8 Iwowa anapita ku Mizipa kwa Gedaliya. Amene anapitawo
ndi awa: Ismaeli mwana wa Netaniya, Yohanani ndi Yonatani ana a
Kareya, Seraya mwana wa Tanihumeti, ana a Efai a ku Netofa, ndi
Yezaniya mwana wa Maaka, iwowo pamodzi ndi anthu awo. 9 Gedaliya
mwana wa Ahikamu, mdzukulu wa Safani, anawalonjeza iwo pamodzi ndi
anthuwo mwalumbiro. Ndipo anati, "Musaope kuwatumikira Ababuloni.
Khalani m'dziko muno, tumikirani mfumu ya ku Babuloni, ndipo zinthu
zidzakuyenderani bwino. 10 Ine ndidzakhala ku Mizipa kuti ndizikuyimiri-
rani kwa Ababuloni amene azidzabwera kwa ife, koma inu muzikolola
vinyo wanu, zipatso zanu, mafuta anu ndi kuzisunga m'mitsuko yanu,
n'kumakhala m'mizinda imene mwalandayo."

11 Nawonso Ayuda onse a ku Mowabu, ku Amoni, ku Edomu ndi
a ku mayiko ena onse anamva kuti mfumu ya ku Babuloni inasiyako
anthu ena ku Yuda ndipo kuti inasankha Gedaliya mwana wa Ahikamu,
mwana wa Safani, kukhala bwanamkubwa wawo. 12 Tsono Ayuda onsewo
anabwerera ku Yuda, ku Mizipa kwa Gedaliya, kuchokera ku mayiko
onse kumene anabalalikira. Ndipo anakolola zipatso zochuluka ndi vinyo
wambiri.

13 Yohanani mwana wa Kareya ndi atsogoleri a ankhondo onse amene
sanadzipereke aja anabwera ku Mizipa kwa Gedaliya 14 ndipo anamufunsa
kuti, "Kodi sukudziwa kuti Baalisi mfumu ya Aamoni watuma Ismaeli
mwana wa Netaniya kuti akuphe?" Koma Gedaliya mwana wa Ahikamu
sanawankhulupirire.

15 Tsono Yohanani mwana wa Kareya, mwamseri anawuza Gedaliya ku
Mizipa kuti, “Loleni ndipite ndikaphe Ismaeli mwana wa Netaniya, ndipo
palibe amene ati adziwe. Akuphereninji ndi kuchititsa Ayuda onse, amene
akuzungulirani kuti abalalike ndi kuti otsala a ku Yuda awonongeke?”

16 Koma Gedaliya mwana wa Ahikamu anawuza Yohanani mwana
wa Kareya kuti, “Usachite zimenezo! Zimene ukunena za Ismaeli ndi
zabodza.”

# 41

1 Pa mwezi wachisanu ndi chiwiri Ismaeli mwana wa Netaniya,
mdzukulu wa Elisama amene anali wa banja laufumu ndiponso mmodzi
wa atsogoleri a ankhondo a mfumu, anabwera ku Mizipa kwa Gedaliya
mwana wa Ahikamu ndi anthu khumi. Pamene ankadya naye kumeneko,
2 Ismaeli mwana wa Netaniya pamodzi ndi anthu khumi aja anayimirira
ndi kupha ndi lupanga Gedaliya mwana wa Ahikamu, mdzukulu wa
Safani. Choncho anapha munthu amene mfumu ya ku Babuloni in-
amusankha kukhala bwanamkubwa wa dzikolo. 3 Ismaeli anaphanso
Ayuda onse amene anali pamodzi ndi Gedaliya ku Mizipa, kuphatikizanso
asilikali a Ababuloni amene anali ku Mizipako.

4 Mmawa mwake, anthu asanadziwe kuti Gedaliya waphedwa,
5 kunafika anthu 80 ochekera ku Sekemu, Silo ndi Samariya, amene
anali atameta ndevu zawo, atang’amba zovala zawo ndi kudzichekacheka.
Iwowa anatenga chopereka cha ufa ndi lubani kuti adzapereke ku
Nyumba ya Yehova. 6 Ismaeli mwana wa Netaniya anachoka ku Mizipa
akulira kupita kukakumana nawo. Atakumana nawo, iye anati, “Bwerani
mudzaonane ndi Gedaliya mwana wa Ahikamu.” 7 Atafika pakati pa
mzinda, Ismaeli mwana wa Netaniya pamodzi ndi anthu amene anali naye
anawapha anthuwo ndi kuwaponya m’chitsime. 8 Koma anthu khumi a
gululo anawuza Ismaeli kuti, “Musatiphe! Tili ndi tirigu ndi barele, mafuta
ndi uchi, zimene tabisa m’munda.” Choncho anawasiya ndipo sanawa-
phere pamodzi ndi anzawo aja. 9 Tsono chitsime chimene anaponyamo
mitembo ya anthu amene anawaphawo pamodzi ndi mtembo wa Gedaliya
chinali chimene mfumu Asa anachikumba poopsedwa ndi Baasa mfumu
ya Israeli. Ismaeli mwana wa Netaliya anachidzaza ndi mitembo.

10 Pambuyo pake Ismaeli anatenga ukapolo anthu ena onse amene anali
ku Mizipa: ana aakazi a mfumu pamodzi ndi ena onse amene anatsalira
kumeneko, amene Nebuzaradani mtsogoleri wa asilikali olonda mfumu
anapatsa Gedaliya mwana wa Ahikamu kuti akhale bwanamkubwa wawo.
Ismaeli mwana wa Netaliya anatenga ukapolo anthuwa ndi kuwoloka
nawo kumapita ku dziko la Aamoni.

11 Pamene Yohanani mwana wa Kareya ndi atsogoleri onse a ankhondo
amene anali naye pamodzi anamva zoyipa zonse zimene Ismaeli mwana
wa Netaniya anachita, 12 anatenga ankhondo awo onse kupita kuka-
menyana ndi Ismaeli mwana wa Netaniya. Anakamupeza kufupi ndi
chidziwe chachikulu cha ku Gibiyoni. 13 Pamene anthu onse amene
Ismaeli anawagwira anaona Yohanani mwana wa Kareya pamodzi ndi
atsogoleri a ankhondo amene anali naye, anasangalala. 14 Anthu onse
amene Ismaeli anawagwira ukapolo ku Mizipa anabwerera ndi kupita
kwa Yohanani mwana wa Kareya. 15 Koma Ismaeli pamodzi ndi anthu
ake asanu ndi atatu, anathawa Yohanani ndi kuthawira kwa Aamoni.

### *Kuthawira ku Igupto*

16 Kenaka Yohanani mwana wa Kareya pamodzi ndi atsogoleri onse a ankhondo amene anali naye anatsogolera anthu onse otsala a ku Mizipa amene anawapulumutsa kwa Ismaeli mwana wa Netaniya atapha Gedaliya mwana wa Ahikamu. Anthu amenewa anali: asilikali, akazi, ana ndi amuna ofulidwa otumikira mfumu amene anawatenga ku Gibiyoni.
17 Ndipo ananyamuka nayima ku Geruti Kimuhamu pafupi ndi Betelehemu
pa ulendo wawo wopita ku Igupto 18 kuthawa Ababuloni. Iwo anaopa
Ababuloniwo chifukwa Ismaeli mwana wa Netaniya anapha Gedaliya mwana wa Ahikamu, amene mfumu ya ku Babuloni inamuyika kukhala bwanamkubwa wa dzikolo.

# 42

1 Atsogoleri onse a ankhondo pamodzi ndi Yohanani mwana wa Kareya ndi Azariya mwana wa Hosayia, ndiponso anthu onse, ana ndi akuluakulu
omwe, anapita 2 kwa mneneri Yeremiya ndipo anamuwuza kuti, "Chonde
imvani dandawulo lathu ndipo mutipempherere anthu otsalafe kwa Yehova Mulungu wanu. Pakuti monga tsopano mukuona, ngakhale kuti kale tinalipo ambiri, koma tsopano ochepa okha ndiye amene atsala.
3 Mupemphere kuti Yehova Mulungu wanu atiwuze kumene tiyenera kupita ndi chimene tiyenera kuchita."

4 Mneneri Yeremiya anawayankha kuti, "Ndamva zimene mwanenazi. Ndithu ndidzapemphera kwa Yehova Mulungu wanu monga momwe mwandipemphera. Ndidzakuwuzani chilichonse chimene Yehova anene ndipo sindidzakubisirani kanthu kalikonse."

5 Ndipo iwo anawuza Yeremiya kuti, "Yehova akhale mboni yoona ndi yokhulupirika yodzatitsutsa ife ngati sitichita mogwirizana ndi chilichonse
chimene Yehova Mulungu adzakutumani kuti mutiwuze. 6 Kaya ndi
zotikomera kapena zosatikomera, ife tidzamvera Yehova Mulungu wathu, amene takutumaniko. Tidzamvera Yehova Mulungu wathu kuti zinthu zidzatiyendere bwino."

7 Patapita masiku khumi, Yehova anayankhula ndi Yeremiya. 8 Choncho
Yeremiya anayitana Yohanani mwana wa Kareya pamodzi ndi atsogoleri onse a ankhondo amene anali naye ndiponso anthu onse, ana ndi
akulu omwe. 9 Yehova, Mulungu wa Israeli amene munanditumako
kuti ndikapereke madandawulo m'dzina lanu akuti, 10 "Ngati mukhala
m'dziko muno, ndiye kuti ndidzakukhazikitsani, osakuchotsani. Inde ndidzakudzalani osakuchotsani pakuti ndi kumva chisoni kwambiri
chifukwa cha mavuto amene ndabweretsa pa inu. 11 Musayiope mfumu
ya ku Babuloni, imene mukuyiopa tsopano. Musachite nayo mantha, akutero Yehova, pakuti Ine ndili nanu ndipo ndidzakupulumutsani
ndi kukulanditsani m'manja mwake. 12 Ndidzakuchitirani chifundo,
ndipo mfumuyonso idzakuchitirani chifundo ndi kukulolani kuti mukhale m'dziko mwanumwanu.

13 "Koma mwina simudzamvera Yehova Mulungu wanu n'kumanena
kuti, 'Ayi ife sitidzakhala m'dziko muno, 14 ndipo ngati mukunena kuti,
'Ayi, koma tidzapita ku Igupto kumene sitidzaonako nkhondo kapena
kumva kulira kwa lipenga kapenanso kusowa chakudya.' 15 Tsono,
inu otsala a ku Yuda, imvani mawu a Yehova. Iye akuti, ngati
mutsimikiza zopita ku Igupto, n'kupitadi kukakhala kumeneko, 16 ndiye
nkhondo imene mukuyiopayo idzakugonjetsani ku Igupto komweko. Njala imene mukuyiopayo idzakupezani ku Igupto komweko ndipo mudzafera

kumeneko. [17] Kunena zoona, onse amene atsimikiza zopita ku Igupto
kuti akakhale kumeneko adzafa ndi nkhondo njala ndi mliri. Palibe
ndi mmodzi yemwe amene adzapulumuke kapena kuthawa mavuto
amene ndidzawagwetsera.' [18] Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa
Israeli akuti, 'Momwe ndinawakwiyira mwaukali anthu okhala mu
Yerusalemu, koteronso ndidzakukwiyirani mukapita ku Igupto. Mudza-
sanduka chinthu chotemberered wa ndi chochititsa mantha, choseketsa
ndi chonyozeka. Malo ano simudzawaonanso.'

[19] "Inu otsala a ku Yuda, Yehova wakuwuzani kuti, 'Musapite ku Igupto.'
Dziwani chinthu ichi: Ine lero ndikukuchenjezani [20] kuti munalakwitsa
kwambiri. Inu munanditumа kwa Yehova Mulungu wanu n'kumati
'Mukatipempherere kwa Yehova Mulungu wathu, n'kudzatiwuza chimene
afuna kuti tichite, ndipo ife tidzachita.' [21] Ine lero ndakuwuzani, koma
inu simukumverabe zonse zimene Yehova Mulungu ananditumа kuti
ndikuwuzeni. [22] Tsono dziwani ichi: mudzafadi ndi nkhondo, njala ndi
mliri kumalo kumene mukufuna mukakhaleko."

# 43

[1] Yeremiya atatsiriza kuwawuza anthuwo mawu onse a Yehova Mulungu
wawo, amene Yehova anamutuma kuti akawawuze, [2] Azariya mwana
wa Hosayia ndi Yohanani mwana wa Kareya pamodzi ndi anthu onse
odzikuza anawuza Yeremiya kuti, "Ukunama iwe! Yehova Mulungu wathu
sanakutume kuti unene kuti, 'Musapite ku Igupto kukakhala kumeneko.'
[3] Koma ndi Baruki mwana wa Neriya amene akukulimbikitsa kuti utiletse
zopita ku Igupto ndi kuti m'malo mwake tidzipereke m'manja mwa
Ababuloni, kuti iwo atiphe kapena kutitenga ukapolo ku Babuloni."

[4] Motero Yohanani mwana wa Kareya ndi atsogoleri onse a ankhondo
pamodzi ndi anthu onse sanamvere lamulo la Yehova loti akhale m'dziko
la Yuda. [5] M'malo mwake, Yohanani mwana wa Kareya ndi atsogoleri
onse a ankhondo anatenga anthu onse otsala a ku Yuda amene anab-
wera kudzakhala m'dziko la Yuda kuchokera ku mayiko onse kumene
anabalalakirako. [6] M'gulu la anthu otengedwalo munali amuna onse, akazi
ndi ana, ana aakazi a mfumu, ndiponso anthu amene Nebuzaradani
mtsogoleri wa asilikali olonda mfumu anawasiya kwa Gedaliya mwana
wa Ahikamu, mdzukulu wa Safani pamodzinso ndi mneneri Yeremiya ndi
Baruki mwana wa Neriya. [7] Kotero anthuwo analowa m'dziko la Igupto
chifukwa anakana kumvera Yehova, nakafika ku Tapanesi.

[8] Ndipo Yehova anayankhula ndi Yeremiya ku Tapanesi kuti, [9] "Tenga
miyala inayi yayikulu ndipo uyikwirire m'dothi pa chiwundo cha polow-
era ku nyumba yaufumu ya Farao ku Tapanesi. Uchite zimenezi Ayuda
onse akuona. [10] Ndipo uwawuze kuti, 'Yehova Wamphamvuzonse,
Mulungu wa Israeli akuti: Ndidzayitana mtumiki wanga Nebukadinezara
mfumu ya ku Babuloni, ndipo adzakhazika mpando wake waufumu pa
miyala imene ndayikwirira apayi. Iye adzafunyulula tenti yake yaufumu
pa miyala imeneyi. [11] Iye adzabwera kudzathira nkhondo Igupto. Iwo
oyenera kufa ndi mliri adzafa ndi mliri, iwo oyenera kutengedwa ukapolo
adzatengedwa ukapolo, ndipo iwo oyenera kufa ndi lupanga adzafa ndi
lupanga. [12] Adzayatsa moto m'nyumba zopembedzera milungu ya Igupto.
Adzayeretsa dziko la Igupto monga momwe m'busa amayeretsera chovala
chake pochotsamo nsabwe. Pambuyo pake adzachoka m'dziko la Igupto
mwa mtendere. [13] Ku Iguptoko adzagwetsa zipilala zachipembedzo za

ku nyumba yopembedzera mulungu wa dzuwa. Adzatentha ndi moto
nyumba za milungu ya ku Igupto.' "

# 44

*Masautso Chifukwa cha Kupembedza Mafano*

1 Uthenga umene Yeremiya analandira wonena za Ayuda onse amene
ankakhala ku Igupto, ku mizinda ya Migidoli, Tapanesi ndi Mefisi,
ndiponso ku Patirosi ndi uwu: 2 "Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu
wa Israeli akuti: Inu mwaona mavuto aakulu amene ndinawabweretsa pa
Yerusalemu ndi mizinda yonse ya Yuda. Lero mizinda yonseyo yasanduka
mabwinja, yopanda munthu wokhalamo. 3 Zimenezi zinachitika chifukwa
cha zoyipa zomwe anachita. Iwo anaputa mkwiyo wanga pofukiza
lubani ndi potumikira milungu ina imene iwo kapena inu ngakhalenso
makolo anu sanayidziwe. 4 Kawirikawiri Ine ndakhala ndikutuma atumiki
anga, aneneri, amene anati, 'Musachite chinthu chonyansachi chimene
Ine ndimadana nacho!' 5 Koma iwo sanamvere kapena kulabadira;
sanatembenuke kusiya zoyipa zawo kapena kuleka kufukiza lubani kwa
milungu ina. 6 N'chifukwa chake mkwiyo wanga unayaka ngati moto
kutentha mizinda ya ku Yuda ndi misewu ya mu Yerusalemu ndi
kuyisandutsa bwinja mpaka lero.
7 "Ndiye tsopano Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli,
akunena kuti, 'Chifukwa chiyani mukufuna kudziwononga chotere? Kodi
mukufuna kuti amuna, akazi, ana ndi makanda onse aphedwe ndi
kuti mu Yuda musatsale ndi munthu mmodzi yemwe? 8 Chifukwa
chiyani mukuputa mkwiyo wanga popembedza mafano pofukiza lubani
kwa milungu ina m'dziko lino la Igupto m'mene mukukhalamo. Kodi
mukuchita zimenezi kuti mudziwononge nokha ndi kuti mudzisandutse
chinthu choseketsa ndi chonyozeka pakati pa mitundu yonse ya dziko
lapansi? 9 Kodi mwayiwala zoyipa zimene anachita makolo anu, mafumu
a ku Yuda ndi akazi awo, ndiponso zoyipa zimene munachita inuyo ndi
akazi anu m'dziko la Yuda ndi m'misewu ya mu Yerusalemu? 10 Koma
mpaka lero simunalape. Simunandilemekeze kapena kumvera malamulo
anga amene ndinayikira inuyo ndi makolo anu.
11 "N'chifukwa chake Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli
akunena kuti, 'Ine ndatsimikiza zobweretsa mavuto pa inu ndi kuwather-
atu anthu a ku Yuda. 12 Ndidzatenga anthu otsala a ku Yuda amene
atsimikiza zopita ku Igupto ndi kukakhala kumeneko. Onse adzathera
ku Igupto. Adzaphedwa ndi lupanga kapena kufa ndi njala. Kuyambira
wamng'ono mpaka wamkulu, adzaphedwa ndi lupanga kapena kufa ndi
njala. Adzasanduka chinthu chotembereredwa ndi chochititsa mantha,
chinthu choseketsa ndi chonyozeka. 13 Ndidzalanga Ayuda okhala ku
Igupto ndi lupanga, njala ndi mliri, ngati mmene ndinalangira anthu
a ku Yerusalemu. 14 Motero mwa anthu amene anapita ku Igupto
palibe ndi mmodzi yemwe adzapulumuke, kapena kukhala ndi moyo,
kapena kubwerera ku Yuda. Palibe amene adzabwerere kupatula othawa
nkhondo.' "
15 Tsono amuna onse amene anadziwa kuti akazi awo ankafukiza
lubani kwa milungu ina, ndiponso akazi onse amene anali pamenepo,
gulu lalikulu la anthu, pamodzi ndi anthu onse amene amakhala ku
Patirosi m'dziko la Igupto, anati kwa Yeremiya, 16 "Ife sitimvera uthenga
umene watiwuza m'dzina la Yehova! 17 Koma tidzachitadi chilichonse

chimene tinanena kuti tidzachita: Tidzafukiza lubani kwa mfumukazi
yakumwamba ndipo tidzayipatsa nsembe yachakumwa ngati mmene tin-
kachitira ifeyo ndi makolo athu, mafumu athu ndi akuluakulu m'mizinda
ya ku Yuda ndi m'misewu ya mu Yerusalemu. Nthawi imeneyo ife
tinali ndi chakudya chochuluka ndipo tinali pabwino, sitimapeza mavuto.
18 Koma kuchokera nthawi imene tinasiya kufukiza lubani ndi kupereka
chopereka cha chakumwa kwa mfumukazi yakumwamba, ifeyo takhala
tikusowa zinthu ndipo takhala tikuphedwa ndi lupanga ndi kufa ndi
njala."

19 Akazi anawonjezera kunena kuti, "Pamene tinkafukiza lubani kwa
mfumukazi yakumwamba ndi kuyipatsa chopereka cha chakumwa,
kodi suja amuna athu ankavomereza mmene timayipangira mfumukazi
yakumwambayo makeke abwino olembapo chinthunzi chake ndi kuyi-
patsa chopereka cha chakumwa?"

20 Yeremiya atamva kuyankha kumeneku anawawuza kuti, 21 "Kodi
mukuganiza kuti Yehova n'kuyiwala kuti inuyo ndi makolo anu, mafumu
anu ndi akuluakulu anu, ndiponso anthu onse, munkafukiza lubani kwa
mafano a m'mizinda ya ku Yuda ndi m'misewu ya mu Yerusalemu?
22 Ndiye Yehova sakanathanso kupirira ndi machitidwe anu ndi zonyansa
zimene munkachita. N'chifukwa chake dziko lanu linasanduka chipululu,
chinthu choopsa ndi chotembereredwa. Dziko lopandamo anthu monga
zilili lero lino. 23 Mavuto awa akugwerani chifukwa munkafukiza lubani
ndipo munkachimwira Yehova pokana kumvera mawu ake ndi kutsatira
malamulo ndi malangizo ake."

24 Kenaka Yeremiya anawuza anthu onse, makamaka akazi kuti,
"Imvani mawu a Yehova, anthu onse a ku Yuda amene muli mu
Igupto. 25 Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti: Inu
ndi akazi anu munalonjeza ndi pakamwa panu, ndipo malonjezowo
mwakwaniritsa. Inu munanena kuti, 'Tidzachita zimene tinalonjeza,
kufukizira lubani mfumukazi yakumwamba ndi kuyipatsa chopereka cha
zakumwa.' Tsopano chitanitu zimene munalonjezazo! Kwaniritsani
malumbiro anu.

"Yambani, chitani zimene munalonjeza! Kwaniritsani malumbiro anu!
26 Koma imvani mawu a Yehova, inu Ayuda nonse amene mukukhala mu
Igupto: Yehova akuti, 'Ine ndikulumbira m'dzina langa lopambana kuti
palibe wochokera ku Yuda amene akukhala mu Igupto amene adzatchule
dzina langa polumbira kuti, 'Pali Ambuye Yehova wamoyo.' 27 Pakuti
ndionetsetsa kuti ndiwachitire choyipa, osati chabwino. Anthu a ku
Yuda amene akukhala ku Igupto adzaphedwa pa nkhondo. Ena adzafa
ndi njala mpaka onse atatheratu. 28 Amene adzapulumuke ku lupanga
ndi kubwerera ku dziko la Yuda kuchokera ku Igupto adzakhala ochepa
kwambiri. Choncho otsala onse a ku Yuda amene anapita kukakhala ku
Igupto adzadziwa kuti mawu woona ndi ati, anga kapena awo.

29 "Ine Yehova ndikukupatsani chizindikiro chakuti ndidzakulangani ku
malo ano. Motero mudzadziwa kuti mawu anga akuti ndidzakulangani
ndi woona. 30 Yehova akuti, 'Ine ndidzamupereka Farao Hofira mfumu
ya Igupto kwa adani ake amene akufuna kumupha, monga momwe
ndinaperekera Zedekiya mfumu ya Yuda kwa Nebukadinezara mfumu ya
ku Babuloni, mdani wake amene ankafuna kumupha.' "

# 45

*Uthenga kwa Baruki*

1 Uwu ndi uthenga umene mneneri Yeremiya anawuza Baruki mwana
wa Neriya m'chaka cha chinayi cha Yehoyakimu mwana wa mwana ya
Yosiya kuti alembe m'buku. 2 "Yehova Mulungu wa Israeli, akunena kwa
iwe Baruki kuti: 3 Iwe unati, 'Kalanga ine! Yehova wawonjezera chisoni pa
mavuto anga. Ine ndatopa ndi kubuwula ndipo sindikupeza mpumulo.' "
4 Koma Yehova akukuwuza kuti, "Ndidzagwetsa chimene ndinamanga
ndipo ndidzazula chimene ndinadzala. Ndidzachita zimenezi m'dziko
lonse. 5 Kodi tsono ukudzifunira wekha zinthu zazikulu? Usadzifunire.
Pakuti ndidzagwetsa mavuto pa anthu onse, koma ndidzasunga moyo
wako kulikonse kumene ungadzapite."

# 46

1 Yehova anamupatsa Yeremiya uthenga wonena za anthu a mitundu
ina.

*Uthenga Wonena za Igupto*

2 Kunena za Igupto:

Yehova ananena za gulu lankhondo la Farao Neko mfumu ya ku Igupto limene Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni analigonjetsa ku Karikemesi ku mtsinje wa Yufurate m'chaka cha chinayi cha Yehoyakimu mwana wa Yosiya mfumu ya Yuda,

3 anati, "Konzani zishango zanu ndi malihawo,
ndipo yambanipo kupita ku nkhondo!
4 Mangani akavalo,
ndipo kwerani inu okwerapo!
Khalani pa mzere
mutavala zipewa!
Nolani mikondo yanu,
valani malaya anu ankhondo!
5 Yeremiya anati: Kodi ndikuona chiyani?
Achita mantha
akubwerera,
ankhondo awo agonjetsedwa.
Akuthawa mofulumirapo
osayang'ananso m'mbuyo,
ndipo agwidwa ndi mantha ponseponse,"
akutero Yehova.
6 Waliwiro sangathe kuthawa
ngakhale wankhondo wamphamvu sangathe kupulumuka.
Akunka napunthwa ndi kugwa
kumpoto kwa mtsinje wa Yufurate.

7 "Kodi ndani amene akukwera ngati Nailo,
ngati mtsinje wa madzi amkokomo?
8 Igupto akusefukira ngati Nailo,
ngati mitsinje ya madzi amkokomo.
Iye akunena kuti, 'Ndidzadzuka ndi kuphimba dziko lapansi;
ndidzawononga mizinda ndi anthu ake.'
9 Tiyeni, inu akavalo!

Thamangani inu magaleta!
Tulukani, inu ankhondo,
ankhondo a ku Kusi ndi Puti amene mumanyamula zishango,
ankhondo a ku Ludi amene mumaponya uta.
10 Koma tsikulo ndi la Ambuye Yehova Wamphamvuzonse;
tsiku lolipsira, lolipsira adani ake.
Lupanga lake lidzawononga ndi kukhuta magazi,
lidzaledzera ndi magazi.
Pakuti Yehova, Yehova Wamphamvuzonse, adzapereka adani ake ngati nsembe
m'dziko la kumpoto m'mbali mwa mtsinje wa Yufurate.

11 "Pita ku Giliyadi ukatenge mankhwala
iwe namwali Igupto.
Wayesayesa mankhwala ambiri koma osachira;
palibe mankhwala okuchiritsa.
12 Anthu a mitundu ina amva za manyazi ako;
kulira kwako kwadzaza dziko lapansi.
Ankhondo akunka nagwetsanagwetsana,
onse awiri agwa pansi limodzi."
13 Uthenga umene Yehova anapatsa mneneri Yeremiya wonena za kub-
wera kwa Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni kudzathira nkhondo
Igupto ndi uwu:
14 "Mulengeze ku Igupto. Mulengeze ku Migidoli.
Mulengezenso ku Mefisi ndi ku Tapanesi.
Muwawuze anthu akumeneko kuti, 'Imani pamalo panu ndi kukhala okonzeka kudziteteza,
chifukwa lupanga lidzawononga zonse zimene muli nazo.'
15 Chifukwa chiyani mulungu wanu wamphamvu uja Apisi wathawa?
Iye sakanatha kulimba chifukwa Yehova anamugwetsa.
16 Ankhondo anu apunthwa ndi kugwa.
Aliyense akuwuza mnzake kuti,
'Tiyeni tibwerere kwathu,
ku dziko kumene tinabadwira,
tithawe lupanga la adani athu.'
17 Kumeneku iwo adzafuwula kuti,
'Farao, mfumu ya ku Igupto mupatseni dzina lakuti,
Waphokoso, Wotaya mwayi wake.'

18 "Pali Ine wamoyo," ikutero Mfumu,
imene dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse,
"wina adzabwera amene ali ngati Tabori phiri lopambana mapiri ena,
ngati phiri la Karimeli loti njoo m'mbali mwa nyanja.
19 Konzani katundu wanu wopita naye ku ukapolo
inu anthu a ku Igupto,
pakuti Mefisi adzasanduka chipululu
ndipo adzakhala bwinja mopanda wokhalamo.

20 "Igupto ali ngati mwana wang'ombe wokongola,
koma chimphanga chikubwera
kuchokera kumpoto kudzalimbana naye.
21 Ngakhale ankhondo aganyu amene ali naye

ali ngati ana ang'ombe onenepa.
Nawonso abwerera m'mbuyo, nathawa pamodzi.
Palibe amene wachirimika.
Ndithu, tsiku la tsoka lawafikira;
ndiyo nthawi yowalanga.
22 Aigupto akuthawa ndi liwu lawo lili ngati la njoka yothawa
pamene adani abwera ndi zida zawo,
abwera ndi nkhwangwa
ngati anthu odula mitengo.
23 Iwo adzadula nkhalango ya Igupto,"
akutero Yehova,
"ngakhale kuti ndi yowirira.
Anthuwo ndi ochuluka kupambana dzombe,
moti sangatheke kuwerengeka.
24 Anthu a ku Igupto achita manyazi
atengedwa ukapolo ndi anthu a kumpoto."
25 Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli, akunena kuti, "Ndili
pafupi kulanga Amoni mulungu wa Tebesi. Ndidzalanganso Farao ndi
Igupto pamodzi ndi milungu yake yonse, mafumu ake ndi onse amene
amamukhulupirira.
26 Ndidzawapereka kwa amene akufuna kuwapha,
ndiye kuti kwa Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni ndi atsogoleri ake
ankhondo. Komabe, m'tsogolomo Igupto adzakhalanso ndi anthu monga
kale," akutero Yehova.
27 "Iwe mtumiki wanga Yakobo, usachite mantha;
usataye mtima, iwe Israeli.
Ndithu Ine ndidzakupulumutsa kuchokera ku mayiko akutali,
ndidzapulumutsanso zidzukulu zako kuchokera ku mayiko kumene
anapita nazo ku ukapolo.
Yakobo adzabwerera ndipo adzakhala motakasuka ndi pa mtendere,
ndipo palibenso wina amene adzamuopsa.
28 Iwe mtumiki wanga Yakobo, usachite mantha,
pakuti Ine ndili nawe," akutero Yehova.
"Ndidzawononogeratu mitundu yonse ya anthu
a ku mayiko kumene ndakupirikitsira,
Koma iwe sindidzakuwononga kotheratu.
Ndidzakulanga iwe ndithu koma moyenerera;
sindidzakulekerera osakulanga."

# 47

*Uthenga Wonena za Afilisti*

1 Uthenga umene Yehova anamupatsa mneneri Yeremiya wonena za
Afilisti, Farao asanathire nkhondo Gaza ndi uwu:

2 Yehova akuti,
"Taonani mmene madzi akubwerera kuchokera kumpoto;
adzasanduka mtsinje wosefukira ndi a mkokomo.
Adzasefukira m'dziko monse ndi kumiza chilichonse m'menemo,
mizinda ndi onse okhala m'menemo.
Anthu adzafuwula;
anthu onse okhala m'dzikomo adzalira
3 akadzamva mgugu wa ng'ombe zazimuna zothamanga,
phokoso la magaleta ake

ndi kulira kwa mikombero yake.
Makolo sadzatembenuka kuti athandize ana awo;
manja awo adzangoti khoba.
4 Pakuti tsiku lafika
lowononga Afilisti onse
ndi kupha onse otsala,
onse amene akanatha kuthandiza Turo ndi Sidoni.
Yehova ali pafupi kuwononga Afilisti,
otsala ochokera ku zilumba za ku Kafitori.
5 Anthu a ku Gaza ameta mipala;
anthu a ku Asikeloni akhala chete.
Inu otsala a ku chigwa,
mudzakhala mukudzichekacheka mpaka liti?

6 "Mukulira kuti, 'Aa, lupanga la Yehova,
kodi udzapumula liti?
Bwerera m'malo ako;
ukhale momwemo ndipo ukhale chete.'
7 Koma lupangalo lidzapumula bwanji
pamene Yehova walilamulira
kuti lithire nkhondo
Asikeloni ndi anthu a m'mbali mwa nyanja?"

# 48

*Uthenga Wonena za Mowabu*

1 Ponena za Mowabu:

Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti,
"Tsoka kwa mzinda wa Nebo, chifukwa wawonongedwa.
Mzinda wa Kiriyataimu wachititsidwa manyazi ndipo wagonjetsedwa;
linga lichititsidwa manyazi ndipo lagumulidwa.
2 Palibenso amene akutamanda Mowabu;
ku Hesiboni anthu anamupanganira zoyipa:
'Bwerani, tiyeni timuwonongeretu kuti asakhalenso mtundu wa anthu.'
Inunso anthu a ku Madimena, adzakukhalitsani chete;
ankhondo adzakupirikitsani.
3 Tamvani mfuwu wa anthu a ku Horonaimu.
Iwo akulira kuti, 'Kusakazika ndi kuwonongeka kwakukulu.'
4 Mowabu wawonongeka;
ana ake ang'onoang'ono akulira kwambiri.
5 Anthu akukwera chikweza cha ku Luhiti,
akulira kwambiri pamene akupita.
Kulira chifukwa cha chiwonongeko kukumveka
pa njira yotsikira ku Horonaimu.
6 Thawani! Dzipulumutseni;
khalani ngati mbidzi ya m'chipululu.
7 Popeza inu munkadalira ntchito zanu ndi chuma chanu,
nanunso mudzatengedwa ukapolo,
ndipo Kemosi adzapita ku ukapolo,
pamodzi ndi ansembe ake ndi akuluakulu ake.
8 Wowononga adzabwera ndi kusakaza mzinda uliwonse,

ndipo palibe mzinda umene udzapulumuke.
Chigwa chidzasanduka bwinja
ndipo malo athyathyathya a pamwamba pa phiri adzawonongedwa
monga Yehova wayankhulira.
9 Mtsineni khutu Mowabu
chifukwa adzasakazika;
mizinda yake idzasanduka mabwinja,
wopanda munthu wokhalamo.

10 "Wotembereredwa munthu amene amagwira ntchito ya Yehova monyinyirika!
Wotembereredwa munthu amene amaletsa lupanga lake kupha anthu!

11 "Mowabu wakhala pa mtendere kuyambira ubwana wake,
ngati vinyo wokhazikika pa masese ake,
osapungulidwa kuchoka mu mtsuko wina kuthira mu mtsuko wina;
iye sanatengedwepo ukapolo.
N'chifukwa chake kukoma kwake n'komwe kuja
ndipo fungo lake silinasinthe.
12 N'chifukwa chake masiku akubwera,"
akutero Yehova,
"pamene ndidzatuma anthu amene amakhuthula vinyo m'mitsuko
ndipo adzamukhutula;
adzakhuthula vinyo yense mitsuko yake
pambuyo pake n'kuphwanya mitsukoyo.
13 Pamenepo Mowabu adzachita manyazi ndi Kemosi,
monga momwe Aisraeli anachitira manyazi
ndi Beteli amene ankamukhutulira.

14 "Kodi munganene bwanji kuti, 'Ife ndife asilikali.
Ife ndife ngwazi, anthu amphamvu pa nkhondo?'
15 Owononga Mowabu ndi mizinda yake abwera ndipo ankhondo adzalowa m'midzi yake;
anyamata ake okongola apita kukaphedwa,"
ikutero Mfumu, imene dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.
16 Kugwa kwa Mowabu kuli pafupi;
masautso ake akubwera posachedwa.
17 Mulireni kwambiri, inu nonse amene mwamuzungulira,
inu nonse amene mumadziwa za kutchuka kwake;
nenani kuti, "Taonani momwe yathyokera ndodo yamphamvu yaufumu ija,
taonani momwe ndodo yaulemu yathyokera!"

18 "Tsikani pa ulemerero wanu
ndipo khalani pansi powuma,
inu anthu okhala ku Diboni,
pakuti wowononga Mowabu
wabwera kudzamenyana nanu,
wasakaza mizinda yanu yotetezedwa.
19 Inu amene mumakhala ku Aroeri,
imani m'mbali mwa msewu ndi kumaonerera.

Funsani mwamuna amene akuthawa ndiponso mkazi amene wapulumuka,
afunseni kuti, 'Kodi chachitika n'chiyani?' "
20 Iwo adzayankha kuti, "Mowabu wachititsidwa manyazi, pakuti wasakazika.
Lirani mwachisoni ndipo fuwulani!
Lengezani ku mtsinje wa Arinoni
kuti Mowabu wawonongedwa.
21 Chiweruzo chabwera ku mizinda ya ku mapiri,
ndiyo Holoni, Yaza, Mefaati,
22 Diboni, Nebo, Beti-Dibilataimu,
23 Kiriyataimu, Beti-Gamuli, Beti-Meoni,
24 Keriyoti ndi Bozira
ndi mizinda yonse ya Mowabu, yakutali ndi yapafupi yomwe.
25 Mphamvu za Mowabu zawonongeka;
mkono wake wathyoka,"
akutero Yehova.

26 "Muledzeretseni Mowabu,
chifukwa anadzikuza powukira Yehova.
Mulekeni Mowabu avivinizike m'masanzi ake;
mulekeni akhale chinthu chomachiseka.
27 Kodi suja Israeli anali kwa iwe ngati chinthu chomachiseka?
Kodi Israeli anapezeka pakati pa akuba
kuti nthawi zonse poyankhula za iye,
iwe uzimupukusira mutu momunyoza?
28 Inu amene mumakhala ku Mowabu,
siyani mizinda yanu ndi kukakhala pakati pa matanthwe.
Khalani ngati nkhunda imene imamanga chisa chake
pa khomo la phanga.

29 "Tamva za kunyada kwa Mowabu,
kunyada kwake n'kwakukulu.
Ndi wodzitama, wonyada ndi wodzitukumula.
Ali ndi mtima wodzikweza.
30 Ine ndikuzidziwa ntchito zake,
akutero Yehova.
Ntchitozo ndi n'zosapindulitsa kanthu.
31 N'chifukwa chake ndidzamulira Mowabu,
ine ndikulira chifukwa cha anthu onse a ku Mowabu,
ndikubuwula chifukwa cha anthu a ku Kiri Heresi.
32 Ndikukhetsa misozi chifukwa cha inu, kupambana momwe ndinalirira Yazeri.
Inu anthu a ku Sibina muli ngati mipesa
imene nthambi zake zatambalala mpaka ku Nyanja;
zafika mpaka ku nyanja ya Yazeri.
Wowononga wasakaza
zipatso zake zachilimwe ndi mpesa.
33 Chimwemwe ndi chisangalalo zatha
ku minda ya zipatso ya ku Mowabu.
Ndaletsa kuchucha kwa vinyo mopsinyira mphesa;
palibe amene akufuwula mokondwa akamapsinya mphesa.
Ngakhale kufuwula kulipo,

koma sikufuwula kwa chimwemwe.

34 “A ku Hesiboni ndi Eleali akulira
ndipo mfuwu wawo ukumveka mpaka ku Yahazi,
kuchokera ku Zowari mpaka ku Horonaimu ndi ku Egilati Selisiya.
Ngakhale madzi a ku Nimurimu aphwa.
35 Ndidzawaletsa anthu a ku Mowabu
kupereka nsembe m’malo awo opembedzera
ndi kufukiza lubani kwa milungu yawo,”
akutero Yehova.
36 “N’chifukwa chake mtima wanga ukulirira Mowabu ngati chitoliro.
Mtima wanga ukulirira anthu a ku Kiri Heresi ngati chitoliro
chifukwa chuma chimene anachipata chatha.
37 Aliyense wameta mutu wake
ndi ndevu zake;
manja a munthu aliyense ndi ochekacheka,
ndipo munthu aliyense wavala chiguduli m’chiwuno mwake.
38 Pa madenga onse a ku Mowabu
ndiponso m’misewu yake
anthu akungolira,
pakuti ndaphwanya Mowabu
ngati mtsuko wopanda ntchito,”
akutero Yehova.
39 “Taonani mmene waphwanyikira! Tamvani momwe akulirira!
Taonani momwe Mowabu wachititsidwira manyazi.
Mowabu wasanduka chinthu chonyozeka,
chinthu chochititsa mantha kwa onse amene amuzungulira.”
40 Yehova akuti,
“Mtundu wina udzachita kuwuluka n’kugwera pa Mowabu ngati chiwombankhanga
chimene chatambalitsa mapiko ake.
41 Mizinda idzagwidwa
ndipo malinga adzalandidwa.
Pa tsiku limenelo mitima ya ankhondo a ku Mowabu
idzakhala ngati mtima wa mayi pa nthawi yake yochira.
42 Mowabu sudzakhala mtundu wa anthu
chifukwa unadzikuza powukira Yehova.
43 Zoopsa, dzenje ndi msampha zikudikira
inu anthu a ku Mowabu,”
akutero Yehova.
44 “Aliyense wothawa zoopsa
adzagwera m’dzenje,
aliyense wotuluka m’dzenje
adzakodwa mu msampha.
Ndigwetsa zimenezi pa Mowabu
pa nthawi ya chilango chake,”
akutero Yehova.

45 “Anthu othawa nkhondo ayima pa mthunzi wa Hesiboni
chifukwa chotopa.
Koma moto wayaka kuchokera ku Hesiboni,
malawi a moto abuka kuchokera ku nyumba ya mfumu Sihoni.
Motowo ukuwononga mapiri a ku Mowabu,

dziko la anthu onyada.
46 Tsoka kwa iwe Mowabu!
Anthu opembedza Kemosi awonongeka.
Ana ako aamuna ndi aakazi
atengedwa ukapolo.

47 "Komabe masiku akutsogolo
ndidzabwezeranso Mowabu chuma chake,"
akutero Yehova.
Chiweruzo cha Mowabu chathera pamenepa.

# 49

*Uthenga Wonena za Aamoni*

1 Yehova ananena izi:

Amoni,
"Kodi Israeli alibe ana aamuna?
Kapena alibe mlowam'malo?
Tsono n'chifukwa chiyani anthu opembedza Moleki alanda dziko la Gadi?
N'chifukwa chiyani anthu ake akukhala m'mizinda ya Gadi?
2 Koma nthawi ikubwera,"
akutero Yehova,
"pamene ndidzamveketse mfuwu wankhondo
ku Raba, likulu la Amoni;
ndipo malo awo opembedzera milungu yawo
adzatenthedwa ndi moto.
Choncho Aisraeli adzalandanso dziko lawo
kuchokera kwa amene anawalanda poyamba dzikolo,"
akutero Yehova.
3 "Lirani, inu anthu a ku Hesiboni chifukwa wowononga uja wafika!
Fuwulani, inu anthu okhala ku Raba!
Valani ziguduli ndi kulira mwamphamvu;
thamangani uku ndi uku m'kati mwa malinga,
chifukwa mulungu wanu Moleki adzapita ku ukapolo,
pamodzi ndi ansembe ake ndiponso akuluakulu ake.
4 Chifukwa chiyani mukunyadira
chigwa chanu,
inu anthu osakhulupirika
amene munadalira chuma chanu n'kumati:
'Ndani angandithire nkhondo?'
5 Ndidzabweretsa zoopsa pa iwe
zochokera kwa onse amene akuzungulira,"
akutero Ambuye, Mulungu Wamphamvuzonse.
"Mudzathawa, ndipo aliyense adzathawitsa moyo wake.
Sipadzapezeka munthu wosonkhanitsanso othawawo.

6 "Komabe pambuyo pake, ndidzabwezera kwawo Aamoni,"
akutero Yehova.

*Uthenga Wonena za Edomu*

7 Yehova Wamphamvuzonse ananena izi za Edomu:
"Kodi nzeru sizikupezekanso ku Temani?
Kodi anzeru analeka kupereka uphungu?

Kodi nzeru zawo zinatheratu?
8 Inu anthu a ku Dedani, thawani,
bwererani ndi kukabisala ku makwalala
chifukwa ndidzagwetsa mavuto pa zidzukulu za Esau
popeza nthawi yawo ya chiweruzo yafika.
9 Kodi anthu othyola mphesa akanafika kwa inu
akanakusiyiraniko mphesa pang'ono pokha?
Anthu akuba akanafika usiku
akanangotengako zimene akuzifuna zokha?
10 Koma ine ndazivula zidzukulu za Esau.
Ndaonetsa poyera malo awo obisalamo,
kotero kuti sadzathanso kubisala.
Ana ake, abale ake pamodzi ndi anansi ake awonongeka.
Palibe wonena kuti,
11 'Siyani ana anu amasiye; Ine ndidzawateteza.
Amayi anu amasiye akhoza kudalira Ine.' "

12 Yehova akuti, "Ngati iwo amene sanali oyenera kulangidwa adzamwa
chikho cha chiweruzo, ndiye muyesa kuti inuyo simudzalangidwa? Ayi
ndithu simudzakhala osalangidwa. Mudzamwa ndithu chikhocho. 13 Ine
ndikulumbira, akutero Yehova, kuti mzinda wa Bozira udzasanduka
bwinja, chinthu chochititsa mantha, chomachiseka ndiponso chotembereredwa. Mizinda yake yonse idzakhala mabwinja mpaka muyaya."

14 Ndamva uthenga wochokera kwa Yehova:
Nthumwi yatumidwa kupita kwa anthu a mitundu ina kukanena kuti,
"Sonkhanani pamodzi kuti muthire nkhondo Edomu!
Konzekerani nkhondo!"

15 "Ndidzakuchepetsani pakati pa anthu a mitundu ina.
Mudzakhala anthu onyozeka pakati pa anthu.
16 Kuopseza kwako kwakunyenga;
kudzikuza kwa mtima wako kwakusocheretsa,
iwe amene umakhala m'mapanga
a m'matanthwe ndi m'mapiri.
Ngakhale utamanga chisa chako pamwamba kwambiri ngati chiwombankhanga,
ndidzakutsitsa pansi kuchokera kumeneko,"
akutero Yehova.
17 "Dziko la Edomu lidzasanduka chinthu chochititsa mantha.
Onse odutsamo adzadabwa ndi kupukusa mitu yawo
chifukwa cha kuwonongeka kwake.
18 Monga momwe anawonongekera Sodomu ndi Gomora,
pamodzi ndi mizinda yake yozungulira,"
akutero Yehova,
"motero palibe munthu
amene adzakhala mu Edomu.

19 "Monga mkango wotuluka ku nkhalango za ku Yorodani
kupita ku malo a msipu wobiriwira,
Ine ndidzapirikitsa anthu a ku Edomu mwadzidzidzi kuchoka m'dziko lawo.
Pambuyo pake ndidzawayikira owalamulira amene ndamufuna Ine.
Kodi ndani wofanana nane, ndipo angatsutsane nane ndani?
Ndipo ndi m'busa uti amene angalimbane nane?"

20 N'chifukwa chake imvani. Izi ndi zimene Ine Yehova
ndakonza zolangira anthu a ku Edomu ndi a ku Temani.
Ngakhale ana omwe adzatengedwa ukapolo
ndipo aliyense adzachita mantha chifukwa cha iwo.
21 Akadzagwa Edomu padzakhala mfuwu waukulu ndipo dziko lapansi lidzanjenjemera;
kulira kwawo kudzamveka mpaka ku Nyanja Yofiira.
22 Taonani, mtundu wina udzachita kuwuluka
n'kudzatera pa Bozira ngati chiwombankhanga chimene chatambalitsa mapiko ake.
Pa tsiku limenelo mitima ya ankhondo a ku Edomu
idzagunda ngati mtima wa mayi pa nthawi yake yochira.

### *Uthenga Wonena za Damasiko*

23 Mawu a Yehova onena za Damasiko ndi awa:
"Anthu a ku Hamati ndi a ku Aripadi akuchita mantha
chifukwa amva nkhani yoyipa.
Mitima yawo yagwidwa ndi mantha
ndipo ali ngati muja ichitira nyanja yosakhazikika.
24 Anthu a ku Damasiko alefuka.
Abwerera m'mbuyo kufuna kuthawa
chifukwa agwidwa ndi mantha aakulu.
Ali ndi nkhawa komanso mantha
ngati za mayi pa nthawi yake yochira.
25 Mzinda wotchuka
ndi wachikondwerero uja wasiyidwa!
26 N'chifukwa chake anyamata ake adzagwa m'misewu ndi kufa;
ankhondo ake onse adzawonongedwa tsiku limenelo,"
akutero Yehova Wamphamvuzonse.
27 "Ndidzatentha malinga a Damasiko;
moto udzanyeketsa nyumba zaufumu za Beni-Hadadi."

### *Uthenga Wonena za Kedara ndi Hazori*

28 Mawu a Yehova onena za Kedara ndi maufumu a ku Hazori, amene
Nebukadinezara mfumu ya Babuloni anawagonjetsa ndi awa:
"Nyamukani mukathire nkhondo ku Kedara.
Kawonongeni anthu a kummawako.
29 Landani matenti awo ndi nkhosa zawo,
ndiye kuti, mutenge nsalu zawo ndi katundu wawo.
Mutengenso ngamira zawo.
Anthu adzafuwula kwa iwo kuti,
'Kuli zoopsa mbali zonse!'

30 "Thawani mofulumira!
Kabisaleni m'makhwawa, inu anthu ku Hazori,"
akutero Yehova.
"Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni wakukonzerani chiwembu;
wakonzekera zoti alimbane nanu.

31 "Nyamukani kathireni nkhondo mtundu wa anthu umene uli pamtendere,
umene ukukhala mosatekeseka,"
akutero Yehova,

“mzindawo ulibe zipata ngakhalenso mipiringidzo;
anthu ake amakhala pa okha.
32 Ngamira zawo zidzafunkhidwa,
ndipo makola a ng’ombe zawo adzalandidwa.
Ndidzabalalitsira ku mphepo zinayi onse amene amameta tsitsi lawo cham’mbali.
Ndidzawagwetsera mavuto kuchokera ku mbali zonse,”
akutero Yehova.
33 “Hazori adzasanduka bwinja,
malo okhalamo nkhandwe
mpaka muyaya.
Palibe munthu amene adzayendemo.”

### *Uthenga Wonena za Elamu*

34 Uthenga umene Yehova anapatsa mneneri Yeremiya wonena za
Elamu, Zedekiya mfumu ya Yuda atangoyamba kulamulira ndi uwu:

35 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
“Taonani, ndidzathyola uta wa Elamu,
umene uli chida chawo champhamvu.
36 Ndidzabweretsa mphepo zinayi pa Elamu
kuchokera ku zigawo zinayi zamlengalenga;
ndidzawabalalitsira ku mphepo zinayi,
ndipo sipadzakhala dziko
limene anthu a ku Elamu sadzafikako.
37 A ku Elamuwo ndidzachititsa mantha pamaso pa adani awo
komanso pamaso pa iwo amene akufuna kuwononga moyo wawo.
Ndidzawagwetsera mkwiyo wanga
ndipo adzakhala pa mavuto,”
akutero Yehova.
“Ndidzawapirikitsa ndi lupanga
mpaka nditawatheratu.
38 Ndidzakhazika mpando wanga waufumu ku Elamu
ndipo ndidzawononga mfumu yake pamodzi ndi akuluakulu ake,”
akutero Yehova.

39 “Komabe m’tsogolomo ndidzabwezera
anthu a ku Elamu dziko lawo,”
akutero Yehova.

## 50

### *Uthenga Wonena za Babuloni*

1 Uthenga umene Yehova anayankhula ndi mneneri Yeremiya wonena
za mzinda wa Babuloni ndi anthu ake ndi uwu:
2 “Lengeza ndi kulalika pakati pa anthu a mitundu ina,
kweza mbendera ndipo ulengeze;
usabise kanthu, koma uwawuze kuti,
‘Babuloni wagwa;
mulungu wawo Beli wachititsidwa manyazi,
nayenso Mariduku wagwidwa ndi mantha.
Milungu yake yagwidwa ndi mantha
ndipo mafano ake adzagwidwa ndi mantha.’
3 Mtundu wa anthu wochokera kumpoto wadzathira nkhondo Babuloni

ndi kusandutsa bwinja dziko lake.
Kumeneko sikudzakhalanso
munthu kapena nyama.

4 “Masiku amenewo, nthawi imeneyo,”
akutero Yehova,
“anthu a ku Israeli ndi anthu a ku Yuda
onse pamodzi adzabwera akulira. Adzafunitsitsa kuchita zimene Yehova Mulungu wawo akufuna.
5 Adzafunsa njira ya ku Ziyoni
ndi kuyamba ulendo wopita kumeneko.
Iwo adzadzipereka kwa Yehova
pochita naye pangano lamuyaya
limene silidzayiwalika.

6 “Anthu anga ali ngati nkhosa zotayika;
abusa awo
anawasocheretsa m’mapiri.
Iwo anayendayenda m’mapiri ndi m’zitunda
mpaka kuyiwala kwawo.
7 Aliyense amene anawapeza anawawononga;
adani awo anati, ‘Ife si olakwa,
chifukwa iwo anachimwira Yehova, amene ali mpumulo wawo weniweni
ndi amene makolo awo anamukhulupirira.’

8 “Thawaniko ku Babuloni;
chokani m’dziko la Ababuloni.
Muyambe inu kutuluka ngati atonde amene amatsogolera ziweto.
9 Taonani, ndidzaukitsa gulu lankhondo lamphamvu la mitundu ina
ndi kubwera nalo kuchokera kumpoto
kudzamenyana ndi Babuloni.
Iwo adzandandalika ankhondo awo ndi kugonjetsa Babuloni.
Mivi yawo ili ngati ya ankhondo aluso,
yosapita padera.
10 Motero Ababuloni adzafunkhidwa;
ndipo onse omufunkha adzakhuta,”
akutero Yehova.

11 “Inu Ababuloni, munawononga anthu anga osankhika.
Ndiye pano mukukondwa, mukusangalala.
Mukulumphalumpha mokondwa ngati mwana wang’ombe wopuntha tirigu
ndiponso mukulira monyada ngati ng’ombe zazimuna.
12 Koma mzinda wanu udzachititsidwa manyazi kwambiri.
Mzinda umene uli ngati mayi wanu udzanyazitsidwa.
Babuloni adzasanduka chitsirizira cha anthu onse.
Mzinda wawo udzakhala ngati thengo, ngati dziko lowuma lachipululu.
13 Chifukwa cha mkwiyo wa Yehova Babuloni adzakhala wopanda anthu
ndipo adzakhala chipululu chokhachokha.
Onse odutsa kumeneko adzachita mantha ndipo azidzangotsonya
chifukwa cha chiwonongeko chake chachikulu.

14 “Inu okoka uta,
konzekani kuti muthire nkhondo mzinda wa Babuloni mbali zonse.
Muponyereni mivi yanu yonse
chifukwa anachimwira Yehova.
15 Mufuwulireni mbali zonse pakuti wagonja.
Nsanja zake zagwa.
Malinga ake agwetsedwa.
Kumeneku ndiko kulipsira kwa Yehova.
Mulipsireni,
mumuchite zomwe iye anachitira anthu ena.
16 Chotsani ku Babuloni munthu wofesa mbewu aliyense,
ndiponso wodula tirigu ndi chikwakwa chake pa nthawi yokolola.
Poona lupanga la ozunza anzawo,
aliyense adzabwerera kwa anthu ake;
adzathawira ku dziko la kwawo.

17 “Aisraeli ali ngati nkhosa zomwe zabalalika
pothamangitsidwa ndi mikango.
Mfumu ya ku Asiriya ndiye inayamba kuwapha Aisraeliwo.
Wotsiriza anali Nebukadinezara
mfumu ya ku Babuloni
amene anachita ngati kuphwanya mafupa ake.”
18 N’chifukwa chake Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti,
“Ndidzalanga mfumu ya ku Babuloni pamodzi ndi dziko lake
monga momwe ndinalangira mfumu ya ku Asiriya.
19 Koma ndidzabwezera Israeli ku msipu wake
ndipo adzadya m’minda ya ku Karimeli ndi Basani;
adzadya nakhuta ku mapiri
a ku Efereimu ndi Giliyadi.
20 Masiku amenewo, nthawi imeneyo,”
akutero Yehova,
“anthu adzafunafuna zolakwa za Israeli
koma sadzapeza n’chimodzi chomwe,
ndipo adzafufuza machimo a Yuda,
koma sadzapeza ndi limodzi lomwe,
chifukwa otsala amene ndawasiya ndidzawakhululukira.

21 “Lithireni nkhondo dziko la Merataimu
ndi anthu okhala ku Pekodi.
Muwaphe ndi lupanga ndi kuwawonongeratu,”
akutero Yehova.
“Chitani zonse monga momwe ndakulamulani.
22 M’dziko muli phokoso la nkhondo,
phokoso la chiwonongeko chachikulu!
23 Taonani m’mene waphwanyikira ndi kuwonongekera
uja amati ndi nyundo ya dziko lonse lapansi.
Mzinda wa Babuloni wasanduka chinthu chochititsa mantha
pakati pa mitundu ina!
24 Ndinakutchera msampha, iwe Babuloni,
ndipo wakodwamo iwe wosazindikira kanthu;
unapezeka ndiponso unakodwa
chifukwa unalimbana ndi Yehova.

25 Yehova watsekula nyumba ya zida zake
ndipo watulutsa zida za ukali wake,
pakuti Ambuye Yehova Wamphamvuzonse ali ndi ntchito yoti agwire
m'dziko la Ababuloni.
26 Mumenyane naye Babuloni mbali zonse.
Anthu ake muwawunjike
ngati milu ya tirigu.
Muwawononge kotheratu
ndipo pasakhale wopulumuka ndi mmodzi yemwe.
27 Iphani ankhondo ake onse.
Onse aphedwe ndithu.
Tsoka lawagwera
pakuti tsiku lawo lachilango lafika.
28 Tikumva anthu othawa nkhondo ochokera ku Babuloni
akulengeza mu Yerusalemu
za kulipsira kwa Yehova Mulungu wathu.
Iye akulipsira chifukwa chowononga Nyumba yake.

29 "Itanani anthu oponya mivi kudzathira nkhondo Babuloni.
Muyitanenso onse amene amakoka mauta.
Mangani misasa ya nkhondo momuzungulira;
musalole munthu aliyense kuthawa.
Muchiteni monga momwe
iye anachitira anthu ena.
Iyeyu ananyoza
Yehova, Woyera wa Israeli.
30 N'chifukwa chake, anyamata ake adzaphedwa m'mabwalo ake;
ankhondo ake onse adzaphedwa tsiku limenelo,"
akutero Yehova.
31 "Taona, ndikukuthira nkhondo, iwe wodzikuzawe,"
akutero Ambuye Yehova Wamphamvuzonse,
"chifukwa tsiku lako lafika,
nthawi yoti ndikulange yakwana.
32 Wodzikuzawe udzapunthwa n'kugwa
ndipo palibe amene adzakudzutse;
ndidzayatsa moto m'mizinda yake
umene udzanyeketsa onse amene amuzungulira."
33 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Anthu a ku Israeli akuzunzidwa,
pamodzi ndi anthu a ku Yuda,
ndipo onse amene anawagwira ukapolo awagwiritsitsa,
akukana kuwamasula.
34 Koma Mpulumutsi wawo ndi wamphamvu;
dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.
Iye adzawateteza molimba pa mlandu wawo
n'cholinga choti abweretse mtendere m'dziko lawo,
koma adzavutitsa okhala ku Babuloni."

35 Yehova akuti,
"Imfa yalunjika pa Ababuloni,
pa akuluakulu ake
ndi pa anthu ake a nzeru!
36 Imfa yalunjika pa aneneri abodza

kuti asanduke zitsiru.
Imfa yalunjika pa ankhondo ake
kuti agwidwe ndi mantha aakulu.
37 Imfa ilunjike pa akavalo ake ndi magaleta ake.
Ilunjikanso pa magulu ankhondo achilendo amene ali pakati pawo
kuti asanduke ngati akazi.
Chiwonongeko chilunjikenso pa chuma chake
kuti chidzafunkhidwe.
38 Chilala chilunjike pa madzi ake
kuti aphwe.
Babuloni ndi dziko la mafano,
ndipo anthu afika poyaluka nawo mafanowo.

39 "N'chifukwa chake nyama zakuthengo ndi afisi zidzakhala kumeneko
ndipo kudzakhalanso akadzidzi.
Kumeneko sikudzapezekako anthu,
ndithu anthu sadzakhalako pa mibado yonse.
40 Monga momwe Mulungu anawonongera Sodomu ndi Gomora
pamodzi ndi mizinda yonse yozungulira,"
akutero Yehova,
"momwemonso palibe amene adzakhale kumeneko;
anthu sadzayendanso m'menemo.

41 "Taonani! Gulu lankhondo likubwera kuchokera kumpoto;
mtundu wa anthu amphamvu pamodzi ndi mafumu ambiri,
wanyamuka kuchokera kumathero a dziko lapansi.
42 Atenga mauta ndi mikondo;
ndi anthu ankhanza ndipo alibe chifundo.
Phokoso lawo likumveka ngati mkokomo wa nyanja.
Akwera pa akavalo awo,
ndipo akonzekera kudzakuthira nkhondo
iwe Babuloni.
43 Mfumu ya ku Babuloni yamva za mbiri yawo,
ndipo yalobodokeratu.
Ikuda nkhawa,
ikumva ululu ngati wa mayi pa nthawi yake yochira.
44 Taonani, monga mkango wochokera ku nkhalango ya ku Yorodani
kupita ku msipu wobiriwira,
momwemonso ine ndidzapirikitsa Babuloni m'dziko lake mwadzidzidzi.
Pambuyo pake ndidzawayikira wowalamulira amene ndamufuna Ine.
Wofanana nane ndani ndipo ndani amene angalimbane nane?
Ndi mtsogoleri wa dziko uti amene anganditengere ku bwalo la milandu?"
45 N'chifukwa chake imvani.
Izi ndi zimene Ine Yehova ndakonza zolangira anthu a ku Babuloni.
Ngakhale ana omwe adzatengedwa ukapolo
ndipo aliyense adzachita mantha chifukwa cha iwo.
46 Akadzagwa Babuloni padzakhala mfuwu waukulu ndipo dziko lapansi lidzanjenjemera,
ndipo kulira kwawo kudzamveka pakati pa mitundu yonse ya anthu.

# 51

1 Yehova akuti,

“Taonani, ndidzadzutsa mphepo yowononga
kuti iwononge Babuloni pamodzi ndi anthu a ku Lebi Kamai.
2 Ndidzatuma alendo ku Babuloni
kudzamupeta ndi kuwononga dziko lake kotheratu.
Iwo adzalimbana naye ku mbali zonse
pa tsiku la masautso ake.
3 Okoka uta musawalekerere
kapena wonyadira chovala chawo chankhondo.
Musawasiye anyamata ake kuti akhale ndi moyo;
koma muwononge ankhondo ake kotheratu.
4 Adzavulazidwa ndi kufera m’dziko la Babuloni
lomwelo ndi m’misewu yawo yomwe.
5 Pakuti Yuda ndi Israeli sanasiyidwe ngati amasiye
ndi Mulungu wawo, Yehova Wamphamvuzonse,
koma ngakhale dziko la Babuloni ndi lodzaza ndi machimo
pamaso pa Woyerayo wa Israeli.

6 “Thawaniko ku Babuloni!
Aliyense apulumutse moyo wake!
Musawonongeke naye pamodzi chifukwa cha machimo ake.
Imeneyi ndi nthawi yoti Yehova amulange;
Yehova adzamulipsira.
7 Babuloni anali ngati chikho cha golide m’dzanja la Yehova;
kuti aledzeretse dziko lonse lapansi.
Mitundu yambiri ya anthu inamwa vinyo wake;
n’chifukwa chake tsopano inachita misala.
8 Babuloni wagwa mwadzidzidzi ndi kusweka.
Mulireni!
Mfunireni mankhwala opha ululu wake;
mwina iye n’kuchira.”

9 Ena anati, “ ‘Ife tinayesa kumupatsa mankhwala Babuloni,
koma sanachire;
tiyeni timusiye ndipo aliyense apite ku dziko la kwawo,
pakuti mlandu wake wafika mpaka mlengalenga,
wafika mpaka kumwamba.’

10 “ ‘Yehova waonetsa poyera kuti ndife osalakwa;
tiyeni tilengeze mu Ziyoni
zimene Yehova Mulungu wathu wachita.’

11 “Yehova wadzutsa mitima ya mafumu a Amedi,
popeza cholinga chake ndi kuwononga Babuloni.
Motero adzalipsira Ababuloni
chifukwa chowononga Nyumba yake.
Ndiye Yehova akuti,
‘Nolani mivi, tengani zishango.’
12 Kwezani mbendera yankhondo kuti muwononge malinga a Babuloni!
Limbitsani oteteza,
ikani alonda pa malo awo,
konzekerani kulalira.
Pakuti Yehova watsimikiza

ndipo adzachitadi zomwe ananena za anthu a ku Babuloni.
13 Inu muli ndi mitsinje yambiri
ndi chuma chambiri.
Koma chimaliziro chanu chafika,
moyo wanu watha.
14 Yehova Wamphamvuzonse analumbira pali Iye mwini kuti:
Ndidzakutumizira adani ochuluka ngati dzombe,
kuti adzakuthire nkhondo ndipo adzafuwula kuonetsa kuti apambana.

15 "Yehova analenga dziko lapansi ndi mphamvu zake;
Iye anapanga dziko lonse ndi nzeru zake
ndipo anayala thambo mwaluso lake.
16 Iye akayankhula, kumamveka mkokomo wamadzi akumwamba.
Iyeyo amabweretsa mitambo kuchokera ku malekezero a dziko lapansi.
Amabweretsa mphenzi pamodzi ndi mvula
ndi kutulutsa mphepo yamkuntho kumalo kumene amasungira.

17 "Anthu onse ndi opusa ndiponso opanda nzeru;
mmisiri aliyense wosula golide akuchita manyazi ndi mafano ake.
Mafano akewo ndi abodza;
alibe moyo m'kati mwawo.
18 Mafanowo ndi achabechabe, zinthu zosekedwa nazo.
Pamene anthuwo azidzaweruzidwa mafanowo adzawonongedwa.
19 Koma Yehova amene ndi Cholowa cha Yakobo sali ngati mafanowo.
Iyeyu ndi Mlengi wa zinthu zonse,
kuphatikizapo mtundu umene anawusankha kuti ukhale anthu ake.
Dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.

20 "Iwe Babuloni ndi ndodo yanga,
chida changa chankhondo.
Ndi iwe ndimaphwanya mitundu ya anthu,
ndi iwe ndimawononga maufumu,
21 ndi iwe ndimaphwanya kavalo ndi wokwerapo,
ndi iwe ndimaphwanya galeta ndi woyendetsa wake.
22 Ndi iwe ndimaphwanya mwamuna ndi mkazi,
ndi iwe ndimaphwanya nkhalamba ndi wachinyamata,
ndi iwe ndimaphwanya mnyamata ndi namwali.
23 Ndi iwe ndimaphwanya m'busa ndi ziweto,
ndi iwe ndimaphwanya mlimi ndi ng'ombe,
ndi iwe ndimaphwanya abwanamkubwa ndi atsogoleri a ankhondo.
24 "Inu mukuona ndidzalanga Babuloni ndi onse amene amakhala
m'dziko la Babuloni chifukwa cha zolakwa zonse anachita ku Ziyoni,"
akutero Yehova.
25 "Taonani, ndikukuzenga mlandu, iwe phiri lowononga,
amene umawononga dziko lonse lapansi,"
akutero Yehova.
"Ndidzatambalitsa dzanja langa pofuna kukulanga,
kukugubuduzira pansi kuchokera pa matanthwe ako,
ndi kukusandutsa kukhala phiri lopserera.
26 Palibe ngakhale ndi mwala wako umodzi umene anthu adzawutenga
kuti awugwiritse ntchito kumangira nyumba,

chifukwa iwe udzakhala chipululu mpaka muyaya,”
akutero Yehova.

27 “Kwezani mbendera ya nkhondo m’dziko!
Lizani lipenga pakati pa mitundu ya anthu!
Konzekeretsani mitundu ya anthu kuti ikamuthire nkhondo;
itanani maufumu awa:
Ararati, Mini ndi Asikenazi kuti adzamuthire nkhondo.
Ikani mtsogoleri wankhondo kuti amenyane naye;
tumizani akavalo ochuluka ngati magulu a dzombe.
28 Konzekeretsani mitundu ya anthu.
Amenewa ndiwo mafumu a Amedi,
abwanamkubwa awo, atsogoleri a ankhondo,
ndiponso ankhondo a mayiko amene amawalamulira, kuti idzathire nkhondo Babuloni.
29 Dziko likunjenjemera ndi kunthunthumira,
chifukwa zidzachitikadi zimene Yehova wakonzera Babuloni;
kusakaza dziko la Babuloni
kuti musapezeke wokhalamo.
30 Ankhondo a ku Babuloni aleka kuchita nkhondo;
iwo angokhala m’malinga awo.
Mphamvu zawo zatheratu;
ndipo akhala ngati akazi.
Malo ake wokhala atenthedwa;
mipiringidzo ya zipata zake yathyoka.
31 Othamanga akungopezanapezana,
amithenga akungotsatanatsatana
kudzawuza mfumu ya ku Babuloni
kuti alande mzinda wake wonse.
32 Madooko onse alandidwa,
malo onse obisalamo alonda atenthedwa ndi moto,
ndipo ankhondo onse asokonezeka.”
33 Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli akuti,
“Babuloni wokongola uja wakhala ngati malo opunthirapo tirigu
pa nthawi yake yopuntha tirigu; A ku Yerusalemu akuti,
Posachedwapa nthawi yake yomukolola ifika.”

34 A ku Yerusalemu akuti, “Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni watiwononga,
watiphwanya,
ndi kutitaya ngati mbiya yopanda kanthu.
Watimeza ngati ng’ona,
wakhuta ndi zakudya zathu zokoma,
kenaka n’kutilavula.”
35 Anthu a ku Ziyoni anene kuti,
“Zankhanza zimene anatichitira ife ziwabwerere Ababuloni.”
Anthu okhala mu Yerusalemu anene kuti,
“Magazi athu amene anakhetsedwa akhale pa amene akukhala ku Babuloni.”
36 N’chifukwa chake Yehova akuti,
“Taona, ndidzakumenyera nkhondo
ndi kukulipsirira;
ndidzawumitsa nyanja yake

ndipo akasupe ake adzaphwa.
37 Motero Babuloni adzasanduka mulu wa nyumba zogumuka,
malo okhala nkhandwe,
malo ochititsa mantha ndi onyozedwa,
malo wopanda aliyense wokhalamo.
38 Anthu ake onse adzabangula ngati mkango,
adzadzuma ngati ana amkango.
39 Ngati achita dyera
ndiye ndidzawakonzera madyerero
ndi kuwaledzeretsa,
kotero kuti adzasangalala,
kenaka n'kugona tulo mpaka muyaya ndipo sadzadzukanso,"
akutero Yehova.
40 "Ine ndidzawatenga
kuti akaphedwe ngati ana ankhosa onenepa,
ngati nkhosa zazimuna ndi mbuzi.

41 "Ndithu Babuloni walandidwa,
mzinda umene dziko lonse lapansi limanyadira wagwidwa!
Taonani, mmene Babuloni wasandukira chinthu chochititsa mantha
pakati pa mitundu ya anthu!
42 Nyanja yakwera ndi kumiza Babuloni;
mafunde ake okokoma aphimba Babuloni.
43 Mizinda yake yasanduka bwinja,
dziko lowuma ndi lachipululu,
dziko losakhalamo wina aliyense,
dziko losayendamo munthu aliyense.
44 Ndidzalanga Beli mulungu wa Ababuloni,
ndidzamusanzitsa zimene anameza.
Mitundu ya anthu sidzapitanso kwa iye.
Malinga a Babuloni agwa.

45 "Tulukani m'Babuloni anthu anga!
Pulumutsani miyoyo yanu!
Thawani mkwiyo woopsa wa Yehova.
46 Musataye mtima kapena kuchita mantha
pamene mphekesera zikumveka m'dziko mwanu.
Chaka ndi chaka pamabuka mphekesera
za ziwawa m'dziko lapansi,
ndiponso yakuti mfumu yakuti ikuthira nkhondo mfumu ina.
47 Pakuti taonani, nthawi ikubwera ndithu
pamene ndidzalanga mafano a ku Babuloni;
dziko lake lonse lidzachita manyazi
ndi ophedwa ake onse adzakhala ngundangunda pakati pake.
48 Pamenepo kumwamba ndi dziko lapansi ndi zonse zili m'menemo
zidzayimba mokondwa chifukwa cha kugwa kwa Babuloni.
Anthu owononga ochokera kumpoto
adzamuthira nkhondo,"
akutero Yehova.

49 "Babuloni anapha anthu ambiri pa dziko lapansi.
Tsono, nawo anthu a ku Babuloni ayenera kuphedwa
chifukwa anapha anthu a ku Yerusalemu.

50 Inu amene munapulumuka ku nkhondo ya Babuloni,
chokani pano ndipo musazengereze!
Kumbukirani Yehova ngakhale muli ku mayiko akutali,
ganizirani za Yerusalemu."

51 Inu mukuti, "Tikuchita manyazi,
chifukwa tanyozedwa
ndipo nkhope zathu zili ndi manyazi,
chifukwa anthu achilendo alowa
malo opatulika a Nyumba ya Yehova."

52 N'chifukwa chake Yehova akuti,
"Masiku akubwera pamene ndidzalanga mafano ake,
ndipo m'dziko lake lonse
anthu ovulala adzabuwula.
53 Ngakhale Babuloni atadzikweza mpaka mlengalenga
ndi kulimbitsa nsanja zake,
ndidzatuma anthu owononga kudzamenyana naye,"
akutero Yehova.

54 "Imvani mfuwu wolira kuchokera ku Babuloni.
Imvani phokoso lachiwonongeko chachikulu
kuchokera m'dziko la Babuloni.
55 Pakuti Yehova akuwononga Babuloni,
ndipo akuthetsa phokoso lake lalikulu.
Mfuwu wa adani ukumveka ngati mkokomo wa madzi ambiri.
Phokoso lawo likunka likwererakwerera.
56 Pakuti wowononga wafika kudzamenyana ndi Babuloni,
ankhondo ake agwidwa,
ndipo mauta awo athyoka.
Paja Yehova ndi Mulungu wobwezera chilango;
adzabwezera kwathunthu.
57 Ndidzaledzeretsa akuluakulu ake pamodzi ndi anzeru ake,
abwanamkubwa ake, atsogoleri a ankhondo pamodzinso ndi ankhondo;
adzagona kwamuyaya osadzukanso,"
akutero Mfumu, amene dzina lake ndi Yehova Wamphamvuzonse.

58 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
"Malinga aakulu a Babuloni adzasalazidwa
ndipo zipata zake zazitali zidzatenthedwa;
mitundu ya anthu inangogwira ntchito pachabe.
Anthu anatopa ndi kumanga zimene tsopano zikupsa ndi moto."

59 Zedekiya mfumu ya Yuda inali ndi phungu wake wamkulu amene
dzina lake linali Seraya mwana wa Neriya chidzukulu cha Maseya.
M'chaka chachinayi cha ulamuliro wake, Zedekiya anapita ndi Seraya ku
Babuloni. Tsono mneneri Yeremiya anamupatsirako uthenga Serayayo.
60 Yeremiya anali atalemba m'buku za masautso onse amene adzafike
pa Babuloni ndi zina zonse zokhudza Babuloni. 61 Yeremiya anawuza
Seraya kuti, "Ukakafika ku Babuloni, ukaonetsetse kuti wawawerengera
anthu onse mawu onsewa. 62 Ndipo ukanene kuti, 'Inu Yehova, mwanena
kuti mudzawononga malo ano, kotero kuti simudzatsala munthu kapena
nyama m'dziko muno; lidzakhala chipululu mpaka muyaya.' 63 Ukakatha
kuwerenga bukuli, ukalimangirire ku mwala ndipo ukaliponye pakati

pa mtsinje wa Yufurate. 64 Ndipo ukanene kuti, ‘Umu ndi mmene
adzamirire Babuloni ndipo sadzadzukanso chifukwa cha masautso amene
adzamugwere.’ ”

Mawu a Yeremiya athera pamenepa.

# 52

*Kuwononongeka kwa Yerusalemu*

1 Zedekiya anali wa zaka 21 pamene analowa ufumu, ndipo analamulira
zaka 11 ku Yerusalemu. Amayi ake anali Hamutali mwana wa Yeremiya
wa ku Libina. 2 Iye anachita zoyipa pamaso pa Yehova, monga momwe
anachitira Yehoyakimu. 3 Chifukwa cha zonse zimene zinachitika ku
Yerusalemu ndi ku Yuda Yehova anakwiyira anthu ake mpaka kuwachotsa
pamaso pake.

Tsono Zedekiya anawukira mfumu ya ku Babuloni.

4 Choncho m’chaka cha chisanu ndi chinayi cha ulamuliro wa Zedekiya,
mwezi wakhumi, pa tsiku la khumi, Nebukadinezara mfumu ya ku Bab-
uloni anabwera ndi ankhondo ake onse kudzathira nkhondo Yerusalemu.
Anamanga misasa ndi mitumbira yankhondo kunja kuzungulira mzin-
dawo. 5 Mzindawo unazingidwa mpaka chaka cha khumi ndi chimodzi
cha ulamuliro wa Mfumu Zedekiya.

6 Pa tsiku lachisanu ndi chinayi la mwezi wachinayi njala inakula
kwambiri mu mzindamo kotero kuti munalibe chakudya choti anthu
n’kudya. 7 Tsono linga la mzindawo linabowoledwa, ndipo ankhondo
onse anathawa. Iwo anatuluka mu mzindamo usiku kudzera pa chipata
cha pakati pa makoma awiri a pafupi ndi munda wa mfumu, ngakhale
kuti Ababuloni anali atazinga mzindawo. Ndipo anathawira ku Araba,
8 koma gulu la ankhondo la ku Babuloni linalondola mfumu Zedekiya ndi
kumupeza m’chigwa cha ku Yeriko. Ankhondo onse anamusiya yekha
nabalalika.

9 Anagwidwa napita naye kwa mfumu ya ku Babuloni ku Ribula m’dziko
la Hamati, kumene anagamula mlandu wake. 10 Ku Ribulako mfumu ya ku
Babuloni inapha ana aamuna a Zedekiya iyeyo akuona; ndiponso inapha
akuluakulu onse a ku Yuda. 11 Ndipo inamukolowola maso Zedekiya, ndi
kumumanga ndi maunyolo a mkuwa n’kupita naye ku Babuloni kumene
inakamuyika m’ndende kuti akhalemo moyo wake wonse.

12 Mwezi wachisanu, pa tsiku lakhumi, chaka cha 19 cha ulamuliro
wa Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni, Nebuzaradani mtsogoleri
wa ankhondo a mfumu, amene amatumikira mfumu ya ku Babuloni,
anabwera ku Yerusalemu. 13 Ndipo anatentha Nyumba ya Yehova,
nyumba ya mfumu ndi nyumba zonse za mu Yerusalemu. Anatentha
nyumba iliyonse. 14 Tsono gulu lonse lankhondo la Ababuloni limene
linali ndi mtsogoleri wa ankhondo a mfumu uja linagwetsa malinga
onse ozungulira Yerusalemu. 15 Nebuzaradani mtsogoleri wa ankhondo
anatenga anthu amene anatsala mu mzindamo, anthu aluso pamodzi ndi
amene anadzipereka kale kwa mfumu ya ku Babuloni kupita nawo ku
ukapolo ku Babuloni. 16 Komabe Nebuzaradani mtsogoleri wa ankhondo
anasiya anthu ena onse osaukitsitsa a m’dzikomo kuti azigwira ntchito
m’minda ya mpesa ndi minda ina.

17 Ababuloni anaphwanya nsanamira za mkuwa, maphaka ndi chimbiya
chamkuwa zimene zinali m'Nyumba ya Yehova. Anatenga mkuwa
wonsewo n'kupita nazo ku Babuloni. 18 Ankhondowo anatenganso mbiya,
zochotsera phulusa, zozimitsira nyale, mbale zofukizira lubani, zikho
pamodzi ndi ziwiya zina zonse za mkuwa zimene ankagwiritsira ntchito
m'Nyumba ya Yehova. 19 Nebuzaradani uja anatenganso mabeseni,
ziwiya zosonkhapo moto, mbale zowazira madzi, zoyikapo nyale, zipande
zofukizira lubani ndi zikho ndi zina zonse zagolide ndi siliva.
20 Nsanamira ziwiri zija, chimbiya, maphaka ndi ng'ombe khumi ndi
ziwiri za mkuwa zochirikizira chimbiyacho zimene mfumu Solomoni
anapangira Nyumba ya Yehova kulemera kwake kunali kosawerengeka.
21 Nsanamira imodzi kutalika kwake kunali mamita asanu ndi atatu,
akazunguliza chingwe inali mamita asanu ndi theka; m'kati mwake
munali bowo ndipo kuchindikala kwake kunali zala zinayi. 22 Pamwamba
pa nsanamira iliyonse panali mutu wamkuwa umene kutalika kwake
kunali mamita awiri. Pozungulira pake panali ukonde ndi makangadza,
zonsezo za mkuwa. Nsanamira inayo inalinso ndi makangadza ake ndipo
inali yofanana ndi inzake ija. 23 M'mbali mwake munali makangadza 96;
makangadza onse pamodzi analipo 100 kuzungulira ukonde onse.
24 Mtsogoleri wa ankhondo uja, anagwira Seraya mkulu wa ansembe ndi
Zefaniya, wachiwiri wa mkulu wa ansembe ndi alonda atatu apachipata.
25 Mu mzindamo anagwiramo mkulu amene ankalamulira ankhondo, ndi
alangizi amfumu asanu ndi awiri. Anagwiranso mlembi wa mtsogoleri
wa ankhondo, amene ankalemba anthu m'dzikomo, pamodzi ndi anthu
ena 60 amene anali mu mzindamo. 26 Nebuzaradani, mtsogoleri wa
ankhondoyo anawatenga onse napita nawo kwa mfumu ya ku Babuloni
ku Ribula. 27 Ku Ribulako, m'dziko la Hamati, mfumu ya ku Babuloniyo
inalamula kuti anthuwo aphedwe.
Motero anthu a ku Yuda anapita ku ukapolo, kutali ndi dziko lawo.
28 Chiwerengero cha anthu amene Nebukadinezara anawatenga kupita
nawo ku ukapolo ndi ichi:

M'chaka cha chisanu ndi chiwiri cha ulamuliro wake, anatenga Ayuda 3,023;
29 m'chaka cha 18 cha ulamuliro wa Nebukadinezara,
anatenga anthu 832 kuchokera mu Yerusalemu;
30 m'chaka cha 23 cha ulamuliro wa Nebukadinezara,
Nebuzaradani, mtsogoleri wa ankhondo a mfumu anagwira Ayuda 745 kupita ku ukapolo.
Onse pamodzi analipo anthu 4,600.

### *Kumasulidwa kwa Yehoyakini*

31 M'chaka chimene Evili-Merodaki analowa ufumu wa Babuloni, iye
anakomera mtima Yehoyakini mfumu ya ku Yuda, namutulutsa m'ndende.
Izi zinachitika pa tsiku la 25 la mwezi wa khumi ndi chiwiri zitatha zaka
37 chitengedwere Yehoyakimu ku ukapolo. 32 Evili-Merodaki anakomera
mtima Yehoyakini, namupatsa malo aulemu kuposa mafumu ena amene
anali naye ku Babuloni. 33 Choncho Yehoyakini analoledwa kuvula zovala
zake za ku ndende ndipo tsiku ndi tsiku ankadya ndi mfumu pa moyo wake
wonse. 34 Tsiku ndi tsiku mfumu ya ku Babuloni inkamupatsa Yehoyakini
phoso lake nthawi yonse ya moyo wake, mpaka pa nthawi ya imfa yake.

# Maliro

## 1

1 Haa! Mzinda uja wasiyidwa wokhawokha,
umene kale unali wodzaza ndi anthu!
Kale unali wotchuka pakati pa mitundu ya anthu!
Tsopano wasanduka ngati mkazi wamasiye.
Kale unali mfumukazi ya onse pa dziko lapansi,
tsopano wasanduka kapolo.

2 Ukulira mowawidwa mtima usiku wonse,
misozi ili pa masaya pake.
Mwa abwenzi ake onse,
palibe ndi mmodzi yemwe womutonthoza.
Abwenzi ake onse amuchitira chiwembu;
onse akhala adani ake.

3 Yuda watengedwa ku ukapolo,
kukazunzika ndi kukagwira ntchito yolemetsa.
Iye akukhala pakati pa anthu a mitundu ina;
ndipo alibe malo opumulira.
Onse omuthamangitsa iye amupitirira,
ndipo alibe kwina kothawira.

4 Misewu yopita ku Ziyoni ikulira,
chifukwa palibe ndi mmodzi yemwe akubwera ku maphwando ake.
Zipata zake zonse zili pululu,
ansembe akubuwula.
Anamwali ake akulira,
ndipo ali m'masautso woopsa.

5 Adani ake asanduka mabwana ake;
odana naye akupeza bwino.
Yehova wamubweretsera mavuto
chifukwa cha machimo ake ambiri.
Ana ake atengedwa ukapolo
pamaso pa mdani.

6 Ulemerero wonse wa mwana wamkazi wa Ziyoni
wachokeratu.
Akalonga ake ali ngati mbawala
zosowa msipu;
alibe mphamvu zothawira
owathamangitsa.

7 Pa masiku a masautso ndi kuzunzika kwake,
Yerusalemu amakumbukira chuma chonse
chimene m'masiku amakedzana chinali chake.
Anthu ake atagwidwa ndi adani ake,
panalibe aliyense womuthandiza.
Adani ake ankamuyang'ana

ndi kumuseka chifukwa cha kuwonongeka kwake.

8 Yerusalemu wachimwa kwambiri
ndipo potero wakhala wodetsedwa.
Onse amene ankamulemekeza pano akumunyoza,
chifukwa aona umaliseche wake.
Iye mwini akubuwula
ndipo akubisa nkhope yake.

9 Uve wake umaonekera pa zovala zake;
iye sanaganizire za tsogolo lake.
N'chifukwa chake kugwa kwake kunali kwakukulu;
ndipo analibe womutonthoza.
"Inu Yehova, taonani masautso anga,
pakuti mdani wapambana."

10 Adani amulanda
chuma chake chonse;
iye anaona mitundu ya anthu achikunja ikulowa m'malo ake opatulika,
amene Inu Mulungu munawaletsa
kulowa mu msonkhano wanu.

11 Anthu ake onse akubuwula
pamene akufunafuna chakudya;
asinthanitsa chuma chawo ndi chakudya
kuti akhale ndi moyo.
"Inu Yehova, taonani ndipo ganizirani,
chifukwa ine ndanyozeka."

12 "Kodi zimenezi mukuziyesa zachabe, inu nonse mukudutsa?
Yang'anani ndipo muone.
Kodi pali mavuto ofanana ndi
amene andigwerawa,
amene Ambuye anandibweretsera
pa tsiku la ukali wake?

13 "Anatumiza moto kuchokera kumwamba,
unalowa mpaka m'mafupa anga.
Anayala ukonde kuti ukole mapazi anga
ndipo anandibweza.
Anandisiya wopanda chilichonse,
wolefuka tsiku lonse.

14 "Wazindikira machimo anga onse
ndipo ndi manja ake anawaluka pamodzi.
Machimowa afika pakhosi panga,
ndipo Ambuye wandithetsa mphamvu.
Iye wandipereka
kwa anthu amene sindingalimbane nawo.

15 "Ambuye wakana
anthu anga onse amphamvu omwe ankakhala nane:
wasonkhanitsa gulu lankhondo kuti lilimbane nane,

kuti litekedze anyamata anga;
m'malo ofinyira mphesa Ambuye wapondereza
anamwali a Yuda.

16 "Chifukwa cha zimenezi ndikulira
ndipo maso anga adzaza ndi misozi.
Palibe aliyense pafupi woti anditonthoze,
palibe aliyense wondilimbitsa mtima.
Ana anga ali okhaokha
chifukwa mdani watigonjetsa.

17 "Ziyoni wakweza manja ake,
koma palibe aliyense womutonthoza.
Yehova walamula kuti abale ake
a Yakobo akhale adani ake;
Yerusalemu wasanduka
chinthu chodetsedwa pakati pawo.

18 "Yehova ndi wolungama,
koma ndine ndinawukira malamulo ake.
Imvani inu anthu a mitundu yonse;
onani masautso anga.
Anyamata ndi anamwali anga
agwidwa ukapolo.

19 "Ndinayitana abwenzi anga
koma anandinyenga.
Ansembe ndi akuluakulu anga
anafa mu mzinda
pamene ankafunafuna chakudya
kuti akhale ndi moyo.

20 "Inu Yehova, onani mmene ine ndavutikira!
Ndikuzunzika m'kati mwanga,
ndipo mu mtima mwanga ndasautsidwa
chifukwa ndakhala osamvera.
M'misewu anthu akuphedwa,
ndipo ku mudzi kuli imfa yokhayokha.

21 "Anthu amva kubuwula kwanga,
koma palibe wonditonthoza.
Adani anga onse amva masautso anga;
iwo akusangalala pa zimene Inu mwachita.
Lifikitseni tsiku limene munalonjeza lija
kuti iwonso adzakhale ngati ine.

22 "Lolani kuti ntchito zawo zoyipa zifike pamaso panu;
muwalange
ngati mmene mwandilangira ine
chifukwa cha machimo anga onse.
Ndikubuwula kwambiri
ndipo mtima wanga walefuka."

# 2

1 Haa, Ambuye waphimba mwana wamkazi wa Ziyoni
ndi mtambo wa mkwiyo wake!
Iye wataya pansi ulemerero wa Israeli
kuchoka kumwamba.
Pa tsiku la mkwiyo wake Iye sanakumbukirenso
popondapo mapazi ake.

2 Ambuye anawononga midzi yonse ya Yakobo mopanda chifundo;
mu mkwiyo wake anagwetsa
malinga a mwana wamkazi wa Yuda.
Anagwetsa pansi mochititsa manyazi
maufumu ndi akalonga ake.

3 Atakwiya kwambiri, Ambuye anathyola
nyanga iliyonse ya Israeli.
Anabweza dzanja lake lamanja
pamene mdani anamuyandikira.
Ambuye anatentha fuko la Yakobo ngati moto wonyeketsa
umene umawononga zinthu zonse zomwe zili pafupi.

4 Wakokera uta wake pa ife ngati ndife adani;
wayimiritsa dzanja lake pa ife ngati ndife adani,
ndipo anapha onse amene tinkawayang'ana monyadira.
Ukali wake ukuyaka ngati moto
pa tenti ya mwana wamkazi wa Ziyoni.

5 Ambuye ali ngati mdani;
wawonongeratu Israeli;
wawonongeratu nyumba zake zonse zaufumu
ndipo wawononga malinga ake.
Iye wachulukitsa kubuma ndi kulira
kwa mwana wamkazi wa Yuda.

6 Wagwetsa malo ake okhalamo ngati khumbi la m'munda;
wawononga malo ake a msonkhano.
Yehova wayiwalitsa Ziyoni
maphwando ake oyikika ndi masabata ake.
Mokwiya kwambiri, Iye ananyoza
mfumu ndi wansembe.

7 Ambuye wakana guwa lake la nsembe
ndipo wasiya malo ake opatulika.
Iye wapereka makoma a nyumba zake zaufumu
kwa mdani wake;
adaniwo anafuwula m'nyumba ya Yehova
ngati kuti ndi pa tsiku la chikondwerero.

8 Yehova anatsimikiza kugwetsa
makoma a mwana wamkazi wa Ziyoni.
Anawayesa ndi chingwe
ndipo sanafune kuleka kuwagwetsa.
Analiritsa malinga ndi makoma;

onse anawononongeka pamodzi.

9 Zipata za Yerusalemu zalowa pansi;
wathyola ndi kuwononga mipiringidzo yake.
Mfumu ndi akalonga ake agwidwa ukapolo pakati pa mitundu ya anthu,
palibenso lamulo,
ndipo aneneri ake sakupeza
masomphenya kuchokera kwa Yehova.

10 Akuluakulu a mwana wamkazi wa Ziyoni
akhala chete pansi;
awaza fumbi pa mitu yawo
ndipo avala ziguduli.
Anamwali a Yerusalemu
aweramitsa mitu yawo pansi.

11 Maso anga atopa ndi kulira,
ndazunzika m'moyo mwanga,
mtima wanga wadzaza ndi chisoni
chifukwa anthu anga akuwononongeka,
chifukwa ana ndi makanda akukomoka
m'misewu ya mu mzinda.

12 Anawo akufunsa amayi awo kuti,
"Kodi tirigu ndi vinyo zili kuti?"
pamene akukomoka ngati anthu olasidwa
m'misewu ya m'mizinda,
pamene miyoyo yawo ikufowoka
m'manja mwa amayi awo.

13 Ndinganene chiyani za iwe?
Ndingakufanizire ndi chiyani,
iwe mwana wamkazi wa Yerusalemu?
Kodi ndingakufanizire ndi yani
kuti ndikutonthoze,
iwe namwali wa Ziyoni?
Chilonda chako ndi chozama ngati nyanja,
kodi ndani angakuchiritse?

14 Masomphenya a aneneri ako
anali abodza ndi achabechabe.
Iwo sanakupulumutse kuti usapite ku ukapolo
poyika poyera mphulupulu zako.
Mauthenga amene anakupatsa
anali achabechabe ndi osocheretsa.

15 Onse oyenda m'njira yako
akukuwombera m'manja;
akugwedeza mitu yawo ndi kukunyodola
iwe mwana wamkazi wa Yerusalemu:
"Kodi mzinda uja ndi uwu umene unkatchedwa
wokongola kotheratu,
chimwemwe cha dziko lonse lapansi?"

16 Adani ako onse akutsekulira pakamwa ndi kukunyoza;
iwo akunyogodola ndi kukukuta mano awo,
ndipo akuti, “Tamumeza.
Tsiku ili ndi lomwe timayembekezera;
tili ndi moyo kuti tilione.”

17 Yehova wachita chimene anakonzeratu;
wakwaniritsa mawu ake,
amene anatsimikiza kale lomwe.
Wakuwononga mopanda chifundo,
walola mdani kuti akondwere chifukwa cha kugwa kwako,
wakweza mphamvu za adani ako.

18 Mitima ya anthu
ikufuwulira Ambuye.
Iwe khoma la mwana wamkazi wa Ziyoni,
misozi yako itsike ngati mtsinje
usana ndi usiku;
usadzipatse wekha mpumulo,
maso ako asaleke kukhetsa misozi.

19 Dzuka, fuwula usiku,
pamene alonda ayamba kulondera;
khuthula mtima wako ngati madzi
pamaso pa Ambuye.
Kweza manja ako kwa Iye
chifukwa cha miyoyo ya ana ako,
amene akukomoka ndi njala
m’misewu yonse ya mu mzinda.

20 Inu Yehova, onani, ndipo ganizirani:
kodi ndani amene mwamuchitirapo zinthu ngati izi?
Kodi amayi adye ana awo,
amene amawasamalira?
Kodi ansembe ndi aneneri awaphere
m’malo opatulika a Ambuye?

21 Anyamata ndi okalamba aligone pamodzi
pa fumbi la m’misewu ya mu mzinda;
anyamata anga ndi anamwali anga
aphedwa ndi lupanga.
Inu Yehova mwawapha pa tsiku la mkwiyo wanu;
mwawapha mopanda chifundo.

22 Ngati momwe mumayitanira pa tsiku la phwando,
chimodzimodzinso mwandiyitanira zoopsa mbali zonse.
Pa tsiku limene Yehova wakwiya
palibe amene angathawe ndi kukhala ndi moyo;
mdani wanga wawononga
onse amene ndinkawasamala ndi kuwalera.

# 3

1 Ine ndine munthu amene ndaona masautso
ndi ndodo ya ukali wake.
2 Wandipititsa kutali ndipo wandiyendetsa
mu mdima osati m'kuwala;
3 zoonadi anandikantha ndi dzanja lake
mobwerezabwereza tsiku lonse.

4 Wakalambitsa khungu langa ndi mnofu wanga,
ndipo waphwanya mafupa anga.
5 Wandizinga ndi kundizungulira
ndi zowawa ndi zolemetsa.
6 Wandikhazika mu mdima
ngati amene anafa kale.

7 Wandimangira khoma kotero kuti sindingathawe,
wandimanga ndi maunyolo.
8 Ngakhale pamene ndifuwula kapena kupempha chithandizo,
amakana pemphero langa.
9 Wanditsekera njira yanga ndi miyala yosema;
ndipo wakhotetsa tinjira tanga.

10 Wandidikirira ngati chimbalangondo,
wandibisalira ngati mkango.
11 Wandikokera pambali ndi kunding'ambang'amba,
ndipo wandisiya wopanda thandizo.
12 Wakoka uta wake
ndipo walunjikitsa mivi yake pa ine.

13 Walasa mtima wanga
ndi mivi ya m'phodo mwake.
14 Ndinakhala choseketsa cha anthu anga onse;
amandinyodola m'nyimbo zawo tsiku lonse.
15 Wandidyetsa zowawa
ndipo wandimwetsa ndulu.

16 Wathyola mano anga ndi miyala;
wandiviviniza m'fumbi;
17 Wandichotsera mtendere;
ndayiwala kuti kupeza bwino n'chiyani.
18 Choncho ndikuti, "Ulemerero wanga wachoka
ndi zonse zimene ndimayembekeza kwa Yehova."

19 Kukumbukira masautso anga ndi kusowa pokhala,
zili ngati zowawa ndi ndulu.
20 Ine ndikuzikumbukira bwino izi,
ndipo moyo wanga wathedwa m'kati mwanga.
21 Komabe ndimakumbukira zimenezi,
n'chifukwa chake ndili ndi chiyembekezo.

22 Ife sitinawonongekeretu chifukwa chikondi cha Yehova ndi chachikulu,
ndi chifundo chake ndi chosatha.

23 Zimaoneka zatsopano mmawa uliwonse;
kukhulupirika kwanu n’kwakukulu.
24 Mu mtima mwanga ndimati, “Yehova ndiye zanga zonse;
motero ndimamuyembekezera.”

25 Yehova ndi wabwino kwa amene amayembekezera Iye,
kwa munthu amene amafunafuna Iyeyo;
26 n’kwabwino kudikira chipulumutso cha
Yehova modekha.
27 N’kwabwino kuti munthu asenze goli
pamene ali wamng’ono.

28 Akhale chete pa yekha,
chifukwa Yehova wamusenzetsa golilo.
29 Abise nkhope yake m’fumbi
mwina chiyembekezo n’kukhalapobe.
30 Apereke tsaya lake kwa iye amene angamumenye,
ndipo amuchititse manyazi.

31 Chifukwa Ambuye satayiratu
anthu nthawi zonse.
32 Ngakhale amabweretsa zowawa, Iye adzawachitira chifundo,
chifukwa chikondi chake ndi chosatha.
33 Pakuti sabweretsa masautso mwadala,
kapena zowawa kwa ana a anthu.

34 Kuphwanya ndi phazi
a m’ndende onse a m’dziko,
35 kukaniza munthu ufulu wake
pamaso pa Wammwambamwamba,
36 kumana munthu chiweruzo cholungama—
kodi Ambuye saona zonsezi?

37 Kodi ndani angayankhule zinthu n’kuchitika
ngati Ambuye sanavomereze?
38 Kodi zovuta ndi zabwino sizituluka
m’kamwa mwa Wammwambamwamba?
39 Kodi n’chifukwa chiyani munthu aliyense wamoyo amadandaula
akalangidwa chifukwa cha machimo ake?

40 Tiyeni tisanthule ndi kuyesa njira zathu,
ndipo tiyeni tibwerere kwa Yehova.
41 Tiyeni tikweze mitima yathu ndi manja athu
kwa Mulungu kumwamba ndipo tinene kuti:
42 “Ife tachimwa ndi kuwukira
ndipo inu simunakhululuke.

43 “Mwadzikuta ndi mkwiyo ndi kutilondola ndipo
mwatitha mopanda chifundo.
44 Mwadzikuta mu mtambo
kotero mapemphero athu sakukufikani.

45 Mwatisandutsa zinyatsi ndi zinyalala
pakati pa mitundu ya anthu.

46 “Adani anthu atitsekulira pakamwa.
47 Ife tadzazidwa ndi mantha pakuti tagwa m’dzenje,
tapasuka ndi kuwonongedwa.”
48 Misozi m’maso mwanga ikungoti mbwembwembwe
chifukwa anthu anga akuwonongedwa.

49 Misozi idzatsika kosalekeza,
ndipo sidzasiya,
50 mpaka Yehova ayang’ane pansi
kuchokera kumwamba ndi kuona.
51 Mtima wanga ukupweteka poona zimenezi
chifukwa cha akazi onse a mu mzinda.

52 Akundisaka ngati mbalame,
amene anali adani anga, popanda chifukwa.
53 Ayesa kundipha pondiponya m’dzenje
ndi kundiponya miyala;
54 madzi anamiza mutu wanga
ndipo ndinkaganiza kuti imfa yayandikira.

55 Ndinayitana dzina lanu Inu Yehova,
kuchokera m’dzenje lozama.
56 Inu munamva kudandaula kwanga. “Mundimvere
kulira kwanga kopempha thandizo.”
57 Munafika pafupi pamene ndinakuyitanani,
ndipo munati, “Usaope.”

58 Inu Ambuye munandiwombola ku mlandu wanga;
munapulumutsa moyo wanga.
59 Yehova, mwaona zoyipa zimene andichitira.
Mundiweruzire ndinu!
60 Mwaona kuzama kwa kubwezera kwawo,
chiwembu chawo chonse pa ine.

61 Inu Yehova mwamva kunyoza kwawo,
chiwembu chawo chonse pa ine,
62 manong’onong’o a adani anga
ondiwukira ine tsiku lonse.
63 Tawaonani! Kaya ali pansi kapena kuyimirira,
akundinyoza mu nyimbo zawo.

64 Inu Yehova, muwabwezere chowayenera,
chifukwa cha zimene manja awo achita.
65 Phimbani mitima yawo,
ndipo matemberero anu akhale pa iwo!
66 Muwalondole mwaukali ndipo
muwawonongeretu pa dziko lapansi.

# 4

1 Haa! Golide wathimbirira,
golide wosalala wasinthikiratu!
Amwazamwaza miyala yokongola ya kumalo opatulika
pamphambano ponse pa mzinda.

2 Haa! Ana a Ziyoni amtengowapatali
amene kale anali ngati golide,
tsopano ali ngati miphika ya dothi,
ntchito ya owumba mbiya!

3 Ngakhale nkhandwe zimapereka bere
kuyamwitsa ana ake,
koma anthu anga asanduka ankhanza
ngati nthiwatiwa m'chipululu.

4 Lilime la mwana lakangamira kukhosi
chifukwa cha ludzu,
ana akupempha chakudya,
koma palibe amene akuwapatsa.

5 Iwo amene kale ankadya zonona
akupemphetsa m'misewu ya mu mzinda.
Iwo amene kale ankavala zokongola
tsopano akugona pa phulusa.

6 Kuyipa kwa anthu anga kunali kwakukulu
kuposa anthu a ku Sodomu,
amene anawonongedwa m'kamphindi kochepa
popanda owathandiza.

7 Akalonga ake anali owala koposa chisanu chowundana
ndi oyera kuposa mkaka.
Matupi awo anali ofiira kuposa miyala ya rubi,
maonekedwe awo ngati miyala ya safiro.

8 Koma tsopano maonekedwe awo ndi akuda kuposa mwaye;
palibe angawazindikire m'misewu ya mu mzinda.
Khungu lawo lachita makwinyamakwinya pa mafupa awo;
lawuma gwaa ngati nkhuni.

9 Amene anaphedwa ndi lupanga aliko bwino kuposa
amene anafa ndi njala;
chifukwa chosowa chakudya cha m'munda
iwowa ankafowoka ndi njala mpaka kufa.

10 Amayi achifundo afika
pophika ana awo enieni,
ndiwo anali chakudya chawo pamene anthu
anga anali kuwonongeka.

11 Yehova wakwaniritsa ukali wake;

wagwetsa pansi mkwiyo wake woopsa.
Ndipo wayatsa moto m’Ziyoni
kuti uwononge maziko ake.

12 Mafumu a pa dziko lapansi sanakhulupirire,
kapena wina aliyense wokhala pa dziko lonse,
kuti adani kapena ankhondo akhoza kulowa
pa zipata za Yerusalemu.

13 Koma izi zinachitika chifukwa cha kuchimwa kwa aneneri ake
ndi mphulupulu za ansembe ake,
amene ankapha anthu osalakwa pakati pawo.

14 Tsopano akungoyendayenda m’misewu ya mu mzinda
ngati anthu osaona.
Iwo ndi odetsedwa kwambiri ndi magazi
palibe yemwe angayerekeze n’kukhudza komwe chovala chawo.

15 Anthu akuwafuwulira kuti, “Chokani! Inu anthu odetsedwa!”
“Chokani! Chokani! Musatikhudze ife!”
Akamathawa ndi kumangoyendayenda,
pakati pa anthu a mitundu yonse amati,
“Asakhalenso ndi ife.”

16 Yehova mwini wake wawabalalitsa;
Iye sakuwalabadiranso.
Ansembe sakulandira ulemu,
akuluakulu sakuwachitira chifundo.

17 Ndiponso maso athu atopa n’kuyang’ana,
chithandizo chosabwera n’komwe,
kuchokera pa nsanja zathu tinadikirira mtundu
wa anthu umene sukanatipulumutsa.

18 Anthu ankalondola mapazi athu,
choncho sitikanayenda m’misewu yathu mu mzinda.
Chimaliziro chathu chinali pafupi, masiku athu anali owerengeka,
chifukwa chimaliziro chathu chinali chitafika.

19 Otilondola akuthamanga kwambiri
kuposa ziwombankhanga mu mlengalenga;
anatithamangitsa mpaka ku mapiri
ndi kutibisalira m’chipululu.

20 Wodzozedwa wa Yehova, mpweya wathu wotipatsa moyo,
anakodwa m’misampha yawo.
Tinaganiza kuti tidzakhala pansi pa mthunzi wake
pakati pa mitundu ya anthu.

21 Kondwera ndi kusangalala, mwana wamkazi wa Edomu.
Iwe amene umakhala m’dziko la Uzi.
Koma iwenso chikho chidzakupeza;
udzaledzera mpaka kukhala maliseche.

22 Iwe mwana wamkazi wa Ziyoni, chilango chako chidzatha;
Iye sadzatalikitsa nthawi yako ya ukapolo.
Koma Yehova adzalanga machimo ako, iwe mwana wamkazi wa Edomu,
ndi kuyika poyera mphulupulu zako.

# 5

1 Inu Yehova, kumbukirani zimene zinatichitikira;
yang'anani ndipo muone kunyozeka kwathu.
2 Apereka cholowa chathu kwa obwera,
nyumba zathu kwa alendo.
3 Takhala amasiye ndi wopanda abambo,
amayi athu ali ngati akazi amasiye.
4 Tiyenera kugula madzi amene timamwa,
nkhuni zathunso n'zogula.
5 Otilondola atigwira pakhosi;
tafowoka ndipo sakutilola kupumula.
6 Tinadzipereka kwa Aigupto ndi kwa Asiriya
kuti tipeze chakudya.
7 Makolo athu anachimwa ndipo anafa kale,
koma chilango chawo chili pa ife.
8 Akapolo akutilamulira,
ndipo palibe ndi mmodzi yemwe angatimasule m'dzanja lawo.
9 Timapeza chakudya chathu poyika miyoyo yathu pa chiswe
chifukwa cha lupanga m'chipululu.
10 Khungu lathu latentha ngati uvuni m'ng'anjo,
chifukwa cha kuwawa kwa njala.
11 Amayi agwiriridwa mu Ziyoni,
ndi anamwali m'mizinda ya Yuda.
12 Akalonga athu akuwapachika pomangirira manja awo,
akuluakulu sakuwalemekeza.
13 Achinyamata akukakamizidwa kupera tirigu;
anyamata akudzandira ndi mitolo ya nkhuni.
14 Akuluakulu anachokapo pa chipata cha mzinda;
achinyamata aleka nyimbo zawo.
15 Chimwemwe chachoka m'mitima yathu;
kuvina kwathu kwasanduka maliro.
16 Chipewa chathu chaufumu chagwa pamutu pathu.
Tsoka kwa ife, chifukwa tachimwa!
17 Mitima yathu yakomoka chifukwa cha zimenezi,
chifukwa cha zinthu zimenezi maso athu sakuona bwino,
18 pakuti phiri la Ziyoni, limene lasanduka bwinja,
nkhandwe zikungoyendayendapo.

19 Inu Yehova, lamulirani kwamuyaya;
mpando wanu waufumu udzakhalabe ku mibadomibado.
20 Chifukwa chiyani mumatiyiwala nthawi zonse?
Chifukwa chiyani mwatitaya nthawi yayitali chotere?
21 Yehova mutitembenuzire kwa Inu, kuti tibwerere;
mukonzenso masiku athu akhale monga akale,
22 pokhapokha ngati mwatitaya kotheratu,

ndi kuti mwatikwiyira kobzola muyeso.

# Ezekieli

*Zolengedwa za Moyo ndi Ulemerero wa Yehova*

1 Tsiku lachisanu la mwezi wachinayi, chaka cha makumi atatu,
ine ndinali pakati pa am'ndende m'mbali mwa mtsinje wa Kebara.
Tsono kumwamba kunatsekuka ndipo ndinaona maonekedwe a Mulungu
m'masomphenya.

2 Pa tsiku lachisanu la mwezi, chaka chachisanu Yehoyakini ali
m'ndende, 3 Yehova anayankhula ndi wansembe Ezekieli, mwana wa Buzi,
m'mbali mwa mtsinje wa Kebara m'dziko la Ababuloni. Dzanja la Yehova
linali pa iye kumeneko.

4 Ndinayang'ana ndipo ndinangoona mphepo yamkuntho ikubwera ku-
chokera kumpoto. Panali mtambo waukulu wozunguliridwa ndi kuwala
ndipo moto unali lawilawi kuchokera mu mtambowo. Pakati pa motowo
pankaoneka ngati mkuwa wonyezimira. 5 M'katikati mwa motowo munali
zinthu zinayi zamaonekedwe a nyama. Thupi lawo limaoneka ngati la
munthu 6 koma chilichonse chinali ndi nkhope zinayi ndiponso mapiko
anayi. 7 Miyendo yake inali yowongoka; mapazi ake anali a ziboda ngati
phazi la mwana wang'ombe. Ndipo zibodazo zinkawala ngati mkuwa
wonyezimira. 8 M'munsi mwa mapiko awo kumbali zonse zinayi, nyamazo
zinali ndi manja a munthu. Zonse zinayi zinali ndi nkhope ndi mapiko,
9 ndipo mapiko awowo anakhudzana. Chilichonse chimapita molunjika
kutsogolo; sizimatembenuka pamene zimayenda.

10 Nkhope zawo zimaoneka motere: Chilichonse chinali ndi nkhope
ya munthu, ndipo mbali ya kumanja chilichonse chinali ndi nkhope
zinayi zosiyana motere: nkhope ya munthu, nkhope ya mkango ku
dzanja lamanja, nkhope ya ng'ombe ku dzanja lamanzere, ndipo kumbuyo
kwake nkhope ya chiwombankhanga. 11 Ndi m'mene zinalili nkhope
zawo. Mapiko awo anali otambasukira mmwamba. Chamoyo chilichonse
chinali ndi mapiko awiri okhudzana ndi mapiko a chinzake. Chinalinso
ndi mapiko ena awiri ophimbira thupi lake. 12 Zamoyozo zinkayenda
molunjika kutsogolo. Kulikonse kumene mzimu umazitsogolera kupita,
nazonso zimapita kumeneko, osatembenuka pamene zikupita. 13 Pakati
pa zamayozo panali chinthu chooneka ngati makala oyaka kapena miyuni
yoyaka. Moto umayendayenda pakati pa zamayozo; wowala kwambiri,
ndipo mphenzi zimatuluka pakati pawo. 14 Zamoyozo zinkathamanga uku
ndi uko ngati kung'anima kwa mphenzi.

15 Pamene ndinali kuyang'ana zamoyozo, ndinangoona mikombero
ndipo pansi pambali pa chamoyo chilichonse panali mkombero umodzi.
16 Maonekedwe a mikomberoyo anali ngati mwala wonyezimira.
Mikombero yonse inali yofanana ndipo mapangidwe awo anali ngati won-
golowanalowana. 17 Mikombero ija poyenda inkatha kupita mbali iliyonse
yomwe zamoyozo zinayang'ana popanda kutembenuka. 18 Marimu a
mikomberoyo anali aatali ndi ochititsa mantha ndipo marimu onse anayi
anali ndi maso ponseponse.

19 Zamoyozo zinkati zikamayenda, mikomberoyo imayendanso m'mbali
mwake; ndipo zamoyozo zinkati zikamakwera mmwamba, mikomberoyo
imakweranso. 20 Kulikonse kumene mzimu wake unkazitsogolera, zamoy-
ozo zinkapita komweko. Ndipo mikombero ija inkapita nawo pamodzi

popeza kuti mzimu wa zamoyozo ndiwo umayendetsa mikombero ija.
21 Zamoyo zija zinkati zikamayenda mikombero imayendanso. Zamoyozo
zimati zikayima, nayonso mikombero inkayima. Zamoyozo zinkati
zikawuluka, mikomberonso imawuluka nazo pamodzi chifukwa mzimu
wa zamoyo zija ndiwo umayendetsa mikombero ija.

22 Pamwamba pa mitu ya zamoyozo panali chinthu chonga thambo,
lowala ndipo kunyezimira kwake ngati galasi loyang'anitsa ku dzuwa,
loyalidwa pamwamba pa mitu yake. 23 Zamoyozo zinatambalitsa mapiko
ake m'munsi mwa thambo lija, mapiko ake ena kumakhudzana, mapiko
awiri kumaphimba thupi lake. 24 Pamene zamoyo zimayenda ndimamva
phokoso la mapiko ake, ngati mkokomo wa madzi ambiri, ngati liwu la
Wamphamvuzonse, ngati phokoso la gulu lankhondo. Zimati zikayima
zinkagwetsa mapiko ake.

25 Ndipo panamveka mawu kuchokera pamwamba pa thambo la pa mitu
ya zamoyo zija. Nthawi iyi n'kuti zamoyozo zitayima ndi kugwetsa pansi
mapiko ake. 26 Pamwamba pa thambo la pa mitu yake panali chinthu
chimene chimaoneka ngati mpando waufumu wopangidwa ndi mwala
wa safiro, ndipo pamwamba pa mpando waufumuwo panali chinthu
chooneka ngati munthu. 27 Ndinaona kuti mmwamba mwa chiwuno
chake munali ngati chitsulo chowala konsekonse ngati moto. M'munsi
mwa chiwuno chake munalinso ngati moto wokhawokha. Kuwala
kwa mphamvu kunamuzungulira munthuyo. 28 Kuwalako kunali ndi
maonekedwe a utawaleza m'mitambo tsiku limene kwagwa mvula.

Umu ndi mmene ulemerero wa Yehova umaonekera. Pamene ndinawuona ndinagwa pansi ndipo ndinamva mawu akundiyankhula.

# 2

### *Kuyitanidwa kwa Ezekieli*

1 Iye anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu, imirira kuti
ndiyankhule nawe." 2 Pamene ankayankhula nane, Mzimu wa Mu-
lungu unalowa mwa ine ndipo unandiyimiritsa, ndipo ndinamva Iye
akundiyankhula.

3 Iye anati, "Iwe mwana wa munthu, Ine ndikukutuma kwa Aisraeli,
mtundu wa anthu owukira umene wandiwukira Ine; Iwo ndi makolo awo
akhala akundiwukira Ine mpaka lero lino. 4 Ndikukutuma kwa anthu
okanika ndiponso nkhutukumve. Ndikukutuma kuti akawawuze zimene
Ine Ambuye Yehova ndikunena. 5 Kaya akamva kaya sakamvera, pakuti
iwo ndi anthu opanduka, komabe adzadziwa kuti mneneri ali pakati pawo.
6 Tsono iwe mwana wa munthu, usachite nawo mantha kapena kuopa
zimene azikanena. Usachite mantha, ngakhale minga ndi mkandankhuku
zikuzinge ndipo ukukhala pakati pa zinkhanira. Usachite mantha ndi
zimene akunena kapena kuopsedwa ndi nkhope zawo, popeza anthuwa
ndi awupandu. 7 Ukawawuze ndithu mawu anga, kaya akamva kaya
sakamva. Paja anthuwa ndi awupandu. 8 Koma iwe mwana wa munthu,
mvetsera zimene ndikukuwuza. Usakhale wowukira ngati iwowo. Tsono
yasama pakamwa pako kuti udye chimene ndikukupatsa."

9 Nditayang'ana ndinangoona dzanja litaloza ine, litagwira mpukutu
wolembedwa. 10 Anawufunyulura pamaso panga. Mpukutu wonse
unali wolembedwa kuseri n'kuseri. Ndipo mawu amene analembedwa
m'menemo anali a madandawulo, maliro ndi matemberero.

# 3

1 Tsono Mulungu anandiwuza kuti, “Mwana wa munthu, idya chimene
ndikukupatsachi. Idya kenaka upite ukayankhule ndi Aisraeli.” 2 Choncho
ndinayasama ndipo anandipatsa mpukutuwo kuti ndidye.
3 Kenaka Iye anandiwuza kuti, “Iwe mwana wa munthu, idya mpukutu
umene ndikukupatsa kuti ukhute.” Choncho ndinadya, ndipo unkatseke-
mera ngati uchi m’kamwa mwanga.
4 Pamenepo Iye anandiwuza kuti, “Iwe mwana wa munthu, pita tsopano
kwa Aisraeli ndipo ukawawuze mawu anga. 5 Sindikukutuma kwa anthu
oyankhula chiyankhulo chachilendo ndi chovuta, koma kwa Aisraeli.
6 Sindikukutuma kwa mitundu yambiri ya anthu oyankhula chiyankhulo
chachilendo ndi chovuta, amene mawu ake sungawamvetse. Ndithu
ndikanakutuma kwa iwowa, bwenzi iwo atakumvera. 7 Koma Aisraeli
sadzakumvera chifukwa iwo sakufuna kumvera Ine. Paja Aisraeli onse
ndi okanika ndiponso a mtima wowuma. 8 Tsono ine ndakhwimitsa
nkhope yako mofanana ndi nkhope zawo. Ndalimbitsanso mutu wako
mofanana ndi mitu yawo. 9 Ine ndidzakusandutsa wolimba ngati mwala
wa dayimondi umene uposa thanthwe lina lililonse kulimba kwake.
Usachite nawo mantha kapena kuopsedwa nawo. Paja anthuwa ndi
awupandu.”
10 Anatinso, “Iwe mwana wa munthu, umvetsetse bwino zimene
ndikukuwuzazi ndipo mawu angawa uwasunge bwino mu mtima
mwako. 11 Tsopano upite kwa Aisraeli anzako amene ali ku ukapolo
ndipo ukayankhule nawo. ‘Kaya akamvera kaya sakamvera,’ koma
uzikawawuza kuti, Ambuye Wamphamvuzonse akuti zakutizakuti.”
12 Pamenepo Mzimu unandinyamula ndipo kumbuyo kwanga ndinamva
liwu lamphamvu ngati chivomerezi chachikulu, lonena kuti, “Utamandike
ulemerero wa Yehova kumene Iye amakhala!” 13 Phokoso ndinkalim-
valo linali la kugundana kwa mapiko a zamoyo ndiponso phokoso la
mikombero ya pambali pake ija, limene linkamveka ngati chivomerezi
chachikulu. 14 Mzimu wa Yehova unandikweza ndi kundinyamula ndipo
ndinachokapo ndili wowawidwa ndi wonyuka mu mtima. Ndipo dzanja
la Yehova linali pa ine mwa mphamvu. 15 Choncho ndinafika kwa
amene anali mu ukapolo ku Telabibu pafupi ndi mtsinje wa Kebara.
Ndinakhala pansi pakati pawo masiku asanu ndi awiri, ndili wothedwa
nzeru kwambiri.

### *Chenjezo kwa Israeli*

16 Atatha masiku asanu ndi awiriwo, Yehova anandiwuza kuti, 17 “Iwe
mwana wa munthu, Ine ndakuyika kuti ukhale mlonda wa Aisraeli. Uziti
ukamva mawu anga, ndiye uzikawachenjeza. 18 Ndikawuza munthu
woyipa kuti, ‘Iwe udzafa ndithu,’ koma iwe osamuchenjeza kapena
kumuyankhula kuti aleke njira zake zoyipa ndi kuti akhale ndi moyo,
munthu woyipayo adzafa mu uchimo wake, koma Ine ndidzakuyimba
mlandu chifukwa cha imfa yake. 19 Koma ukamuchenjeza munthu woyipa
koma iye osatembenuka mtima kuleka zoyipa zake kapena kusiya njira
zake zoyipa, munthuyo adzafa chifukwa cha uchimo wake koma iwe
udzapulumutsa moyo wako.
20 “Ngati munthu wolungama asiya chilungamo chake ndi kuchita
uchimo ndipo Ine n’kumuyika m’zoopsa, munthuyo adzafa ndithu.
Popeza iwe sunamuchenjeze, adzafadi chifukwa cha tchimo ndipo
chilungamo chake sichidzakumbukiridwa, koma ndidzakuyimba mlandu

chifukwa cha imfa yake. 21 Koma ngati umuchenjeza munthu wolungama
kuti asachimwe ndipo iye n'kuleka kuchimwa adzakhala ndi moyo ndithu
chifukwa anamvera chenjezo, ndipo iwe udzapulumutsa moyo wako."

22 Nthawi ina dzanja la Yehova linali pa ine ndipo anandiwuza kuti,
"Nyamuka upite ku chigwa, kumeneko ndikayankhula nawe." 23 Choncho
ndinanyamuka kupita ku chigwa. Ndipo ndinaona ulemerero wa Yehova
kumeneko, ngati ulemerero umene ndinaona m'mbali mwa mtsinje wa
Kebara ndipo ndinagwa pansi chafufumimba.

24 Koma Mzimu wa Mulungu unalowa mwa ine ndipo unandiyimir-
itsa. Tsono Yehova anandiyankhula nati: "Pita, kadzitsekere m'nyumba
mwako. 25 Ndipo iwe mwana wa munthu, adzakumanga ndi zingwe
motero kuti sudzatha kuyendanso pakati pa anthu. 26 Ndidzamatirira
lilime lako kukhosi, kotero kuti udzakhala chete wosatha kuwadzudzula,
chifukwa iwo ndi anthu aupandu. 27 Koma pamene ndidzayankhula
kwa iwe, ndidzatsekula pakamwa pako ndipo udzawawuza kuti, 'Ambuye
Yehova akuti zakutizakuti.' Aliyense wofuna kumva amve ndipo wokana
kumva, muleke akane; pakuti iwo ndi anthu opanduka."

# 4

### *Chionetsero cha Kuzingidwa kwa Yerusalemu*

1 Mulungu anati, "Iwe mwana wa munthu, tsopano tenga njerwa, uliyike
pamaso pako ndipo ujambulepo chithunzi cha mzinda wa Yerusalemu.
2 Ndipo uwuzinge mzindawo motere: uwumangire nsanja zowuzinga,
uwumbire mitumbira ya nkhondo, uwumangire misasa ya nkhondo ndipo
uyike zida zogumulira kuzungulira mzindawo. 3 Kenaka utenge chiwaya
chachitsulo uchiyike ngati khoma lachitsulo pakati pa iwe ndi mzindawo.
Uyang'anitsitse mzindawo ndipo udzakhala wozingidwa ndi nsanja za
nkhondo. Choncho umangire nsanja zankhondo. Chimenechi chidzakhala
chizindikiro kwa Aisraeli.

4 "Tsono iwe ugonere kumanzere kwako ndipo ndidzayika pa iwe tchimo
la Aisraeli. Iwe udzasenza tchimolo masiku onse amene udzagonere mbali
imeneyo. 5 Ine ndakuyikira masiku okwana 390 malingana ndi zaka za
machimo awo. Umu ndi mmene udzasenzere machimo a Aisraeli.

6 "Utatha zimenezo udzagonerenso mbali ya kudzanja lamanja, ndipo
udzasenza machimo a anthu a ku Yuda masiku makumi anayi, tsiku
lililonse kuyimira chaka chimodzi. 7 Tsono udzayang'anitsitse nsanja za
nkhondo zozinga. Dzanja la mkanjo wako utalikwinya ndi dzanja lako
utakweza, udzalosere modzudzula Yerusalemu. 8 Ine ndidzakumanga ndi
zingwe kotero kuti sudzatha kutembenukira uku ndi uku mpaka utatsiriza
masiku akuzingidwa ako.

9 "Tsono tenga tirigu ndi barele, nyemba ndi mphodza, mapira ndi
mchewere; ndipo uyike zonsezi m'mbale imodzi ndipo upange buledi
wako. Uzidya pa masiku 390 amene udzakhala ukugonera mbali imodzi.
10 Uyeze theka la kilogalamu la chakudyacho kuti uzidya tsiku lililonse
kamodzi kokha. 11 Uyezenso zikho ziwiri zamadzi ndipo uzimwa tsiku
ndi tsiku. 12 Uzidya chakudya chako ngati momwe amadyera keke ya
barele. Uzidzaphika chakudyacho anthu akuona pogwiritsa ntchito ndowe
ya munthu ngati nkhuni." 13 Yehova anati, "Chimodzimodzi anthu a
Israeli adzadya chakudya chodetsedwa ku mayiko achilendo kumene Ine
ndidzawapirikitsira."

14 Koma ine ndinati, "Zisatero, Ambuye Yehova! Ine sindinadziyipitsepo
pa zachipembedzo. Kuyambira ubwana wanga mpaka tsopano, sindi-
nadyepo kanthu kalikonse kopezeka katafa kapena kophedwa ndi zirombo
za kutchire. Palibe nyama yodetsedwa pa zachipembedzo imene inalowa
pakamwa panga."
15 Iye anati, "Chabwino, ndidzakulola kuti uphike buledi wako ndi
ndowe za ng'ombe m'malo mwa ndowe za munthu."
16 Pambuyo pake anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu, anthu a ku
Yerusalemu ndidzawachepetsera chakudya. Anthuwo adzadya chakudya
chochita kuyeza ndipo azidzadya mwa nkhawa. Azidzamwanso madzi
ochita kuyeza ndiponso mwa mantha. 17 Ndidzachita zimenezi kuti adza-
sowe chakudya ndi madzi. Choncho adzachita nkhawa akumapenyana
ndipo adzatheratu ndi kuwonda chifukwa cha machimo awo."

# 5

*Chizindikiro cha Chiweruzo*

1 Tsiku lina Yehova anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu, tsopano
tenga lupanga lakuthwa ndipo uligwiritse ntchito ngati lumo lometera.
Umete tsitsi ndi ndevu zako. Kenaka utenge sikelo ndipo ugawe tsitsilo
patatu. 2 Kuzinga mzinda kuja kukatha, chimodzi cha zigawo zitatu za
tsitsilo uchitenthe pakati pa mzinda. Chigawo chachiwiri uchiduledule
ndi lupanga, poyenda muzungulire mzinda wonsewo. Chigawo chachitatu
uchimwazire ku mphepo, ndidzachitsata nditasolola lupanga. 3 Koma
utengeko tsitsi pang'ono, ulimange mu mpindiro wa mkanjo wako. 4 Pa
tsitsi limeneli utapepo lina, uliponye pa moto ndi kulitentha. Moto
udzayambira pamenepo mpaka ku nyumba yonse ya Israeli."
5 Ambuye Yehova akunena kuti, "Uyu ndi Yerusalemu amene ndamuyika
pakati pa mitundu ya anthu, ndipo mayiko onse amuzungulira. 6 Koma
anthu a Yerusalemu aphwanya malamulo anga pochita zoyipa kuposa
anthu a mitundu ina. Iwo anandipandukira kupambana anthu ena amene
awazungulira. Iwo anakana malamulo anga ndipo sanasunge malangizo
anga.
7 "N'chifukwa chake Ambuye Yehova akuti: Popeza mwakhala os-
amvera kupambana anthu a mitundu ina amene akuzungulirani, popeza
simunatsate malamulo anga kapena kusunga malangizo anga, m'malo
mwake mwakhala mukutsata makhalidwe a anthu a mitundu ina amene
akuzungulirani.
8 "Tsono Ambuye Yehova akuti: Ine mwini ndikutsutsana nawe,
Yerusalemu, choncho Ine ndidzakulangani. Ine ndidzakulangani anthu
a mitundu ina akuona. 9 Chifukwa cha ntchito zanu zonyansa ndidza-
kulangani ndi chilango chimene sindinakulangeni nacho n'kale lomwe
ndipo sindidzakulangani ndi chofanana nacho m'tsogolomo. 10 Tsono
pakati panu makolo adzadya ana awo, ndipo ana adzadya makolo
awo. Ndidzakulanga ndipo otsala onse ndidzawabalalitsa ku mphepo
zonse zinayi. 11 Ndithu, pali Ine, akutero Ambuye Yehova Wamoyo,
pakuti mwayipitsa Nyumba yanga ndi mafano ano oyipa ndi miyambo
yanu yonyansa, Inenso ndidzakulangani. Sindidzakulekererani kapena
kukumverani chisoni. 12 Chimodzi mwa zigawo zitatu za anthu ako
chidzafa ndi mliri, kapena chidzawonongeka ndi njala; chigawo china
chidzaphedwa ndi lupanga kunja kwa mzinda, ndipo chigawo china
ndidzachibalalitsira ku mphepo zonse zinayi pochita kuchithamangitsa.

13 “Ndi mmene udzachitire mkwiyo wanga. Ndikadzatsiriza kuwalanga,
pamenepo mtima wanga udzakhala pansi. Adzadziwa kuti Ine Yehova
ndinawayankhula mwa nsanje ndikadzawalanga.
14 “Ndidzakusandutsa iwe bwinja ndi chinthu chonyozeka pakati pa
anthu a mitundu ina amene akuzungulira, ndi kwa onse odutsapo
15 Udzakhala chinthu chonyozeka ndi chonyogodoledwa. Udzakhala
chenjezo ndi chinthu choopsa kwa anthu a mitundu ina amene akuzun-
gulira ndikadzakulanga mokwiya ndi mwaukali ndi kugamula mlandu
wako mokwiya. Ine Yehova ndayankhula. 16 Pamene ndidzakulasa ndi
njala yolasa ngati mivi yoopsa ndi yosakaza ndidzatero n’cholinga choti
ndikuwonongeni. Ndidzagwetsa njalayo pa iwe mowirikiza pochepetsa
chakudya chako cha tsiku ndi tsiku. 17 Ndidzatumiza njala ndi zirombo
za kuthengo, ndipo zidzakulanda ana ako. Mliri ndi kuphana zidza-
khala pakati pako, ndipo ndidzakubweretsera nkhondo. Ine Yehova
ndayankhula.”

# 6

*Uneneri Wotsutsa Mapiri a Israeli*

1 Yehova anandipatsa uthenga uwu kuti, 2 “Iwe mwana wa munthu,
yang’ana ku mapiri a Israeli; yankhula nawo modzudzula 3 kuti, ‘Inu
mapiri a ku Israeli, imvani mawu a Ambuye Yehova. Iye akuwuza mapiri,
magomo, mitsinje ndi zigwa kuti: Ine ndizakuthirani nkhondo ndipo
ndidzawononga nyumba zanu m’mene mukupembedzeramo mafano.
4 Maguwa anu ansembe adzagumulidwa ndipo maguwa anu ofukizira
lubani adzaphwanyidwa; ndipo ndidzapha anthu anu pamaso pa mafano
anu. 5 Ine ndidzagoneka mitembo ya Aisraeli pamaso pa mafano awo,
ndipo ndidzamwaza mafupa anu mozungulira maguwa anu ansembe.
6 Konse kumene mumakhala, mizinda yanu idzasanduka bwinja. Nyumba
zanu zopembedzera mafano zidzagumulidwa kotero kuti maguwa anu
adzawonongedwa ndi kusakazidwa, mafano anu adzaphwanyidwa ndi
kuwonongedwa. Maguwa anu ofukizirapo lubani adzagwetsedwa pansi
ndipo zonse zimene munapanga zidzatheratu. 7 Anthu anu adzaphedwa
pakati panu, ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.’
8 “Komabe ndidzasiya ena pang’ono opulumuka ku nkhondo. Iwowa
ndidzawamwazira ku mayiko ena pakati pa anthu a mitundu ina.
9 Pamenepo opulumuka mwa inu adzandikumbukira ku mayiko
kumene anatengedwa ukapolo. Ndidzawamvetsa chisoni chifukwa cha
kusakhulupirika kwawo ndi kundipandukira kuja ndiponso chifukwa
kuti anayika mtima wawo pa mafano. Choncho adzachita okha
manyazi chifukwa cha zoyipa zimene ankachita ndi miyambo yonyansa
imene ankatsata. 10 Ndipo iwo adzadziwa kuti ndine Yehova ndi kuti
sindinkawaopseza chabe pamene ndinanena kuti ndidzawawononga.
11 “Ambuye Yehova akuti: Womba m’manja mwako ndipo uponde
mapazi ako pansi mwamphamvu ndipo ufuwule kuti, ‘Mayo!’ chifukwa
cha zonyansa ndi zoyipa zonse zimene Aisraeli achita, pakuti adzaphedwa
ndi lupanga, njala ndi mliri. 12 Amene ali kutali adzafa ndi mliri, ndipo
amene ali pafupi adzafa pa nkhondo, ndipo amene adzapulumuke ndi
kusaphedwa adzafa ndi njala. Kotero ndidzakwaniritsa ukali wanga pa
iwo. 13 Ndipo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, pamene anthu
awo adzagona atafa pakati pa mafano awo mozungulira maguwa awo

ansembe, pamwamba pa magomo ndi mapiri onse, pansi pa mtengo uliwonse watambalala ndi wa thundu uliwonse wamasamba ambiri, kumalo kumene ankapereka nsembe zonunkhira kwa mafano awo onse.
14 Choncho ndidzawalanga ndi mkono wanga ndi kusandutsa dziko kukhala bwinja. Dziko lonse kumene akukhala kuyambira ku chipululu mpaka ku mzinda wa Ribula ndidzalisandutsa bwinja. Pamenepo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

# 7

*Chimaliziro Chafika*

1 Yehova anandipatsa uthenga uwu kuti, 2 "Iwe mwana wa munthu, Ine
Ambuye Yehova ndikuwuza dziko la Israeli kuti:
"Chimaliziro! Chimaliziro chafika
ku ngodya zinayi za dziko.
3 Chimaliziro chili pa iwe tsopano.
Mkwiyo wanga ndidzawuthira pa iwe.
Ndidzakuweruza molingana ndi machitidwe ako
ndi kukulanga chifukwa cha zonyansa zako.
4 Ine sindidzakumvera chisoni
kapena kukuleka.
Ndidzakulanga ndithu chifukwa cha ntchito zako zoyipa
komanso chifukwa cha miyambo yako yonyansa imene ili pakati pako.
Pamenepo udzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

5 "Zimene ndikunena Ine Ambuye Yehova ndi izi:
"Chiwonongeko! Chiwonongeko chimene sichinamvekepo!
Taona chikubwera!
6 Chimaliziro chafika!
Chimaliziro chafika!
Chiwonongeko chakugwera.
Taona chafika!
7 Inu anthu okhala m'dziko,
chiwonongeko chakugwerani.
Nthawi yafika, tsiku layandikira; tsiku la chisokonezo osati la chimwemwe
pa mapiri.
8 Ine ndili pafupi kukukwiyirani,
ndipo ukali wanga udzathera pa iwe;
Ine ndidzakuweruza molingana ndi machitidwe ako
ndiponso ndidzakulanga chifukwa cha miyambo yako yonyansa.
9 Ine sindidzakumvera chisoni
kapena kukuleka.
Ndidzakulanga malingana ndi ntchito zako
ndiponso chifukwa cha miyambo yako yonyansa pakati pako.
'Pamenepo udzadziwa kuti Ine Yehova ndine amene ndimakantha.'

10 "Taona, tsikulo!
Taona, lafika!
Chiwonongeko chako chabwera.
Ndodo yaphuka mphundu za maluwa.
Kudzitama kwaphuka.
11 Chiwawa chasanduka ndodo
yowakwapulira chifukwa cha kuyipa kwawo.

Palibe mwa anthu amenewo amene adzatsale.
Palibe ndi mmodzi yemwe mwa unyinji wawo.
Palibiretu ndipo sipadzapezeka
munthu wowalira maliro.
12 Nthawi yafika!
Tsiku layandikira!
Munthu wogula asakondwere
ndipo wogulitsa asamve chisoni,
popeza ukali wanga uli pa gulu lonse.
13 Wogulitsa sadzazipezanso zinthu
zimene anagulitsa kwa wina
chinkana onse awiri akanali ndi moyo,
pakuti chilango chidzagwera onsewo
ndipo sichingasinthike.
Chifukwa cha machimo awo, palibe aliyense
amene adzapulumutsa moyo wake.

14 “Lipenga lalira,
ndipo zonse zakonzeka.
Koma palibe ndi mmodzi yemwe amene akupita ku nkhondo,
pakuti mkwiyo wanga uli pa gulu lonse.
15 Ku bwalo kuli kumenyana
ndipo m’kati muli mliri ndi njala.
Anthu okhala ku midzi
adzafa ndi nkhondo.
Iwo okhala ku mizinda
adzafa ndi mliri ndi njala.
16 Onse amene adzapulumuka
ndi kumakakhala ku mapiri,
azidzalira ngati nkhunda za ku zigwa.
Aliyense azidzabuwula chifukwa cha machimo ake.
17 Dzanja lililonse lidzalefuka,
ndipo bondo lililonse lidzalobodoka ngati madzi.
18 Iwo adzavala ziguduli
ndipo adzagwidwa ndi mantha.
Adzakhala ndi nkhope zamanyazi
ndipo mitu yawo adzameta mpala.

19 “Iwo adzataya siliva wawo m’misewu
ndipo golide wawo adzakhala chinthu chonyansa.
Siliva ndi golide wawo
sizidzatha kuwapulumutsa
pa tsiku la ukali wa Yehova.
Chuma chawochi sichidzawathandiza kuthetsa njala,
kapena kukhala okhuta,
pakuti ndicho chinawagwetsa m’machimo.
20 Iwo ankanyadira zodzikongoletsera zawo zamakaka
ndipo ankazigwiritsa ntchito kupanga mafano awo onyansa ndi zonyansa zawo zina.
N’chifukwa chake Ine ndidzazisandutsa
kukhala zowanyansa.
21 Ndidzazipereka kwa alendo kuti azifunkhe.
Anthu oyipa a dziko lapansi adzazilanda

ndi kudziyipitsa.
22 Ine ndidzawalekerera anthuwo
ndipo adzayipitsa malo anga apamtima.
Adzalowamo ngati mbala
ndi kuyipitsamo.

23 "Konzani maunyolo,
chifukwa dziko ladzaza ndi anthu opha anzawo
ndipo mzinda wadzaza ndi chiwawa.
24 Ndidzabweretsa mitundu ya anthu oyipitsitsa
kuti idzalande nyumba zawo.
Ndidzathetsa kunyada kwa anthu amphamvu
pamene anthu akunja adzalowa m'malo awo achipembedzo ndi kuyipitsamo.
25 Nkhawa ikadzawafikira
adzafunafuna mtendere koma osawupeza.
26 Tsoka lidzatsatana ndi tsoka linzake,
ndipo mphekesera idzatsatana ndi mphekesera inzake.
Iwo adzayesa kufuna masomphenya kuchokera kwa mneneri.
Adzasowa ansembe owaphunzitsa malamulo,
ndipo anthu akuluakulu sadzakhalanso ndi uphungu.
27 Mfumu idzalira,
kalonga adzagwidwa ndi mantha.
Manja a anthu a m'dzikomo azidzangonjenjemera ndi mantha.
Ine ndidzawalanga molingana ndi machitidwe awo,
ndipo ndidzawaweruza molingana ndi momwe anaweruzira anzawo.
Choncho adzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

# 8

## *Kupembedza Mafano M'nyumba ya Mulungu*

1 Tsiku lachisanu la mwezi wachisanu ndi chimodzi, m'chaka
chachisanu ndi chimodzi, ndinakhala m'nyumba mwanga pamodzi ndi
akuluakulu a ku Yuda. Tsono mphamvu za Ambuye Yehova zinandifikira.
2 Nditayang'ana ndinangoona chinthu chooneka ngati munthu. Kuchokera
pamene pamaoneka ngati chiwuno chake kumatsika m'munsi anali
ngati moto, ndipo kuchokera m'chiwuno kukwera mmwamba amaoneka
mowala ngati mkuwa wonyezimira. 3 Iye anatambasula chinthu chooneka
ngati dzanja ndipo anagwira tsitsi la pamutu panga. Nthawi yomweyo
Mzimu unandikweza mlengalenga. Tsono ndikumachita ngati ndikuona
Mulungu kutulo, Mzimu uja unapita nane ku Yerusalemu nundiyika pa
khomo la chipata cham'kati choyang'ana kumpoto. Kumeneko kunali fano
limene limaputa mkwiyo wa Mulungu. 4 Kumeneko ndinaona ulemerero
wa Mulungu wa Israeli ngati momwe ndinaonera m'masomphenya
m'chigwa muja.

5 Tsono Yehova anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu, tayang'ana
kumpoto." Choncho ndinayang'ana kumpoto ndipo ndinaona pa khomo
la chipata pafupi ndi guwa lansembe ndinaona fano loputa mkwiyo wa
Mulungu lija.

6 Ndipo Yehova anandifunsa kuti, "Iwe mwana wa munthu, kodi ukuona
zimene akuchitazi, zonyansa zazikulu zimene Aisraeli akuchita kuno,
zinthu zondichotsa Ine kumalo anga opatulika? Koma iwe udzaona zinthu
zimene zili zonyansa kwambiri."

7 Kenaka Iye anandipititsa ku khomo lolowera ku bwalo la Nyumba ya
Mulungu. Nditayang'anitsitsa ndinangoona dzenje pa khomapo. 8 Yehova
anandiwuza kuti, “Iwe mwana wa munthu, tsopano bowola pa khomapo.”
Ndinabowoladi pa khomapo ndipo ndinapezapo khomo.

9 Ndipo Yehova anandiwuza kuti, “Lowa, ndipo ona zinthu zonyansa
zimene akuchita pamenepa.” 10 Motero Ine ndinalowa ndi kuyang'ana,
ndipo ndinaona pa makoma onse zithunzi za zinthu zosiyanasiyana
zokwawa pansi, za nyama zonyansa ndiponso za mafano onse amene
Aisraeli ankapembedza. 11 Patsogolo pa zimenezi panayima akuluakulu
makumi asanu ndi awiri a Aisraeli, ndipo Yaazaniya mwana wa Safani
anali atayima pakati pawo. Aliyense wa iwo anali ndi chofukizira lubani
m'dzanja lake ndipo utsi wa fungo lokoma la lubani unkafuka.

12 Tsono Yehova anandifunsa kuti, “Iwe mwana wa munthu, kodi waona
zimene akuluakulu a Aisraeli akuchita mu mdima, aliyense akupembedza
fano lakelake m'nyumbamo? Iwo akuti, ‘Yehova sakutiona; Yehova
walisiya dziko!’ 13 Iye anandiwuzanso kuti, ‘Iwe udzawaonanso akuchita
zinthu zonyansa kwambiri.’ ”

14 Kenaka anapita nane pa khomo la ku khomo la chipata cha Nyumba
ya Mulungu choyang'ana kumpoto, ndipo kumeneko ndinaona akazi ena
atakhala pansi, akulira mulungu wawo wotchedwa Tamuzi. 15 Yehova
anandifunsa kuti, “Iwe mwana wa munthu, kodi ukuziona zimenezi? Iwe
udzaona zinthu zimene zili zonyansa kwambiri kuposa izi.”

16 Kenaka Iye anapita nane m'kati mwa bwalo la Nyumba ya Yehova.
Kumeneko ku khomo lolowera ku Nyumba ya Yehova pakati pa khonde
ndi guwa lansembe, panali amuna 25. Anafulatira Nyumba ya Mulungu
wa Yehova ndipo nkhope zawo zinaloza kummawa, ndipo ankapembedza
dzuwa choyang'ana kummawa.

17 Yehova anandifunsa kuti, “Iwe mwana wa munthu, kodi waziona
zimenezi? Kodi n'chinthu chopepuka kuti anthu a ku Yuda azichita
zonyansa zimene akuchitazi pano? Kodi afike mpaka pomafalitsa za
ndewu m'dziko lonse? Iwotu akuwutsa ukali wanga. Akundipsetsa
mtima ndi zochita zawo! 18 Choncho Ine ndidzawalanga ndili wokwiya.
Sindidzawamvera chisoni kapena kuwaleka. Ngakhale atandifuwulira
m'makutu mwanga sindidzawamvera.”

# 9

*Opembedza Mafano Aphedwa*

1 Pambuyo pake Yehova anandiyankhula mofuwula kuti, “Bwerani
pafupi, inu odzalanga mzindawu, aliyense ali ndi chida chake m'manja.”
2 Ndipo ndinaona anthu asanu ndi mmodzi akubwera kuchokera ku
chipata chakumtunda chimene chimaloza kumpoto, aliyense ali ndi chida
choopsa cha nkhondo m'dzanja lake. Pagulu pawopa panali munthu
wovala chovala chabafuta, atatenga zolembera pambali pake. Iwo
analowa ndi kuyima pambali pa guwa lamkuwa.

3 Tsono ulemerero wa Mulungu wa Israeli unakwera kuchokera
pamwamba pa akerubi, pamene unali, ndipo unafika pa chiwundo cha
Nyumba ya Mulungu. Pamenepo Yehova anayitana munthu amene
anavala chovala chabafuta uja amene anatenga zolembera pambali pake
4 ndipo anamuwuza kuti, “Pita mu mzinda wonse wa Yerusalemu ndi

kuyika chizindikiro pamphumi pa anthu amene akumva chisoni ndi kulira chifukwa cha zinthu zonse zonyansa zimene zikuchitika mu mzindamo."
5 Kenaka ndinamva Yehova akuwuza anthu ena aja kuti, "Mutsateni mu mzinda wonse ndipo mukakanthe aliyense mopanda kumvera chisoni
kapena chifundo. 6 Mukaphe kotheratu anthu okalamba, anyamata ndi
atsikana, makanda ndi akazi koma musakakhudze wina aliyense amene ali ndi chizindikiro. Muyambire ku Nyumba yanga yopatulika." Motero iwo anayamba ndi akuluakulu amene anali kutsogolo kwa Nyumba ya Mulungu.
7 Ndipo Yehova anawawuza kuti, "Ipitsani Nyumba ya Mulungu ndipo mudzaze mabwalo ake ndi anthu akufa. Pitani." Choncho iwo anapita
nayamba kupha anthu mu mzinda monse. 8 Pamene iwo ankapha
anthu, ine ndinatsala ndekha. Tsono ndinadzigwetsa chafufumimba ndi kufuwula kuti, "Aa, Ambuye Yehova! Kodi mwawakwiyiratu anthu a ku Yerusalemu motero kuti mudzawononga kotheratu anthu onse otsala ku Israeli?"
9 Iye anandiyankha kuti, "Tchimo la Aisraeli ndi Yuda ndi lalikulu kwambiri; dziko ladzaza ndi zophana ndipo mu mzinda mwadzaza ndi zosalungama. Iwo akunena kuti, 'Yehova walisiya dziko lake; Yehova
sakuona.' 10 Choncho sindidzawamvera chisoni kapena kuwaleka, koma
Ine ndidzawalanga potsata zochita zawo."
11 Ndipo munthu wovala chovala chabafuta uja atatenga zolembera pambali pake anadzafotokozera Yehova kuti, "Ndachita monga munandilamulira."

# 10

*Ulemerero Uchoka ku m'Nyumba ya Mulungu*

1 Ine nditayang'ana ku thambo limene lili pamwamba pa mitu ya akerubi ndinangoona chinthu chooneka ngati mpando waufumu wa
mwala wa safiro. 2 Tsono Yehova anawuza munthu wovala chovala
chabafuta uja kuti, "Pita pakati pa mikombero kunsi kwa akerubi. Udzaze manja ako ndi makala oyaka amene ali pakati pa akerubiwo ndipo uwawaze mu mzinda." Iye anachita zimenezi ine ndikuona.
3 Apa akerubiwo anali atayima mbali ya kummwera kwa Nyumba ya Mulungu pamene munthuyo ankalowa. Tsono mtambo unadzaza bwalo
lam'kati. 4 Ndipo ulemerero wa Yehova unachoka pamwamba pa akerubi
ndipo unafika ku chiwundo cha Nyumba ya Mulungu. Mtambo unadzaza Nyumba ya Mulungu, ndipo kuwala kwa ulemerero wa Yehova kunadzaza
bwalolo. 5 Phokoso la mapiko a akerubi limamveka mpaka ku bwalo
lakunja, monga momwe linamvekera liwu la Mulungu Wamphamvuzonse akamayankhula.
6 Kenaka Yehova analamula munthu wovala chovala chabafuta uja kuti, "Pala moto pakati pa mikombero, pakati pa akerubi." Munthu uja
anapitadi nakayima pa mbali pa mkombero umodzi. 7 Ndipo mmodzi wa
akerubi anatambalitsa dzanja lake mpaka pa moto umene unali pakati pawo. Iye anapalako motowo ndipo anapatsa munthu wovala chovala
chabafuta uja. Tsono iye anawulandira natuluka. 8 Ndiye kuti kunsi kwa
mapiko akerubi kumaoneka zinthu zooneka ngati manja a munthu.
9 Ine nditayang'anitsitsa ndinaona mikombero inayi pambali pa akerubi. Pambali pa kerubi aliyense panali mkombero umodzi; mikomberoyo
inkanyezimira ngati miyala yokongola ya krizoliti. 10 Maonekedwe a

mikombero inayi ija anali ofanana. Mkombero uliwonse umaoneka
ngati mkombero wolowana ndi unzake. [11] Poyenda akerubiwo, amapita
mbali iliyonse ya mbali zinayizo kumene akerubiwo amayang'ana.
Mikomberoyo simatembenuka pamene akerubiwo ankayenda. Kulikonse
kumene mutu walunjika n'kumene ankapita popanda kutembenuka.
[12] Matupi awo onse, misana yawo, manja awo ndi mapiko awo zinali
ndi maso okhaokha, monganso m'mene inalili mikombero yawo inayi ija.
[13] Ine ndinamva mikombero ikutchedwa kuti, "mikombero yakamvulu-
vulu." [14] Kerubi aliyense anali ndi nkhope zinayi. Nkhope yoyamba inali
ya Kerubi, nkhope yachiwiri inali ya munthu, nkhope yachitatu inali ya
mkango ndipo nkhope yachinayi inali ya chiwombankhanga.

[15] Tsono akerubi aja anawuluka. Izi zinali zamoyo zija zimene
ndinaziona ku mtsinje wa Kebara. [16] Pamene akerubi ankayenda,
nayonso mikombero ya m'mbali mwawo inkayenda. Akerubiwo ankati
akatambasula mapiko awo kuti auluke mikombero sinkachoka m'mbali
mwawo. [17] Akerubiwo ankati akayima, mikombero inkayimanso. Ngati
akerubiwo auluka, mikomberoyo inkapita nawo chifukwa mzimu wa
zamoyozo ndiwo unkayendetsa mikomberoyo.

[18] Pamenepo ulemerero wa Yehova unachoka pa chiwundo cha Nyumba
ya Mulungu ndi kukakhala pamwamba pa akerubi. [19] Ine ndikuona
akerubi, anatambasula mapiko awo ndi kuwuluka. Pamene ankapita,
mikombero inapita nawo pamodzi. Akerubi anakayima pa khomo la
chipata cha kummawa cha Nyumba ya Yehova. Tsono ulemerero wowala
wa Mulungu wa Israeli unali pamwamba pawo.

[20] Izi ndizo zamoyo ndinaziona pansi pa Mulungu wa Israeli ku mtsinje
wa Kebara, ndipo ndinazindikira kuti anali akerubi. [21] Kerubi aliyense
anali ndi nkhope zinayi ndi mapiko anayi, ndipo kunsi kwa mapiko awo
kunali chinthu chimene chimaoneka ngati manja a munthu. [22] Nkhope
zawo zinali zofanana ndi zomwe ndinaziona ku mtsinje wa Kebara.
Kerubi aliyense amayenda molunjika.

# 11

*Chiweruzo pa Atsogoleri a Israeli*

[1] Pamenepo Mzimu wa Mulungu unandinyamula ndi kubwera nane ku
chipata cha kummawa cha Nyumba ya Yehova. Kumeneko pa khomo
la chipata panali anthu 25, ndipo ndinaona pakati pawo atsogoleri awa:
Yaazaniya mwana wa Azuri ndi Pelatiya mwana wa Benaya. [2] Yehova
anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu, awa ndi anthu amene
akukonza zoyipa ndi kupereka malangizo oyipa mu mzindamo. [3] Iwo
amawuza anthu kuti, 'Nthawi sinafike yoti timange Nyumba? Mzindawu
uli ngati m'phika umene uli pa moto ndipo ife tili ngati nyama mu
m'phikamo. [4] Choncho iwe mwana wa munthu, unenere mowadzudzula.
Nenera ndithu.' "

[5] Ndipo Mzimu wa Yehova unandigwera ndipo unandiwuza kuti, "Unene
kuti zimene akunena Yehova ndi izi. Iye akuti. 'Izi ndi zimene mukunena,
Inu Aisraeli, koma Ine ndikudziwa zimene zili mu mtima mwanu.'
[6] Mwapha anthu ambiri mu mzinda muno ndipo mwadzaza misewu yake
ndi mitembo.

[7] "N'chifukwa chake Ambuye Yehova akuti, 'Mitembo imene
mwayiponya m'misewuyo ndiyo nyama ndipo mzinda uno ndiwo
m'phika, koma Ine ndidzakuthamangitsanimo. [8] Inu mumaopa lupanga,

koma lupangalo ndi limene ndidzakubweretsereni, akutero Ambuye.
9 Ine ndidzakuthamangitsani mu mzinda ndipo ndidzakuperekani
m'dzanja la alendo kuti akulangeni. 10 Mudzaphedwa ndi lupanga ndipo
ndidzakulangani mpaka kumalire a Israeli. Pamenepo mudzadziwa kuti
Ine ndine Yehova. 11 Mzinda uno sudzakhala ngati m'phika wokutetezani
ndipo simudzakhalanso ngati nyama ya m'menemo. Ndidzakulangani
mpaka kumalire a Israeli. 12 Ndipo inu mudzadziwa kuti Ine ndine
Yehova. Inu simunatsatire malangizo anga kapena kusunga malamulo
anga koma mwakhala mukutsata zochita za mitundu ina ya anthu imene
yakuzungulirani.' "

13 Tsono pamene ndinkanenera, Pelatiya mwana wa Benaya anafa.
Pomwepo ndinadzigwetsa pansi chafufumimba ndipo ndinafuwula ndi
mawu aakulu kuti "Mayo, Ambuye Yehova! Kodi mudzawatheratu Aisraeli
onse otsala?"

14 Yehova anayankhula nane kuti, 15 "Anthu okhala ku Yerusalemu
akuwanena abale ako, anthu a ku ukapolo, onse a banja la Israeli, kuti,
'Anthu onse amene anatengedwa ukapolo ali kutali ndi Yehova. Dziko
lanu Yehova anatipatsa kuti likhale lathulathu.' "

### *Mulungu Alonjeza za Kubwerera kwa Israeli*

16 "N'chifukwa chake nena kwa anzako a ku ukapolo kuti, 'Ambuye
Yehova akuti: Ine ndinawatumiza kutali pakati pa anthu a mitundu ina.
Ndinawabalalitsa ku mayiko ambiri. Komabe ndakhala ndikuwasunga ku
mayiko kumene anapitako!'

17 "N'chifukwa chake uwawuze zimene Ine Ambuye Yehova ndikunena
kuti, Ndidzawasonkhanitsa kuchokera kwa anthu a mitundu inayo ndi
kuwasonkhanitsira pamodzi kuchokera ku mayiko kumene ndinawabal-
alitsirako. Pambuyo pake ndidzawapatsa dziko la Israeli.

18 "Akadzalowa m'dzikomo adzachotsa mafano awo onse oyipa ndi
onyansa. 19 Ndidzawapatsa mtima watsopano ndipo ndidzayika mzimu
watsopano mwa iwo. Ndidzachotsa mtima wowuma ngati mwala mwa
iwo, ndipo ndidzawapatsa mtima wofewa ngati mnofu. 20 Motero
adzatsata malamulo anga ndipo adzasunga mosamala malamulo anga.
Adzakhala anthu anga, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wawo. 21 Koma
kunena za amene akupembedza mafano oyipa ndi onyansa, ndidza-
walanga chifukwa cha zimene achita. Ndikutero Ine Ambuye Yehova."

22 Tsono akerubi aja anatambasula mapiko awo kuyamba kuwuluka,
mikombero ili m'mbali mwawo. Ulemerero wa Mulungu wa Israeli
unali pamwamba pawo. 23 Ulemerero wa Yehova unakwera ndi
kusiya mzindawo ndipo unakayima pa phiri cha kummawa kwake kwa
mzindawo. 24 Pambuyo pake Mzimu wa Mulungu unandinyamula ndi
kukandifikitsa. Zimenezi zinkachitika m'masomphenya monga mmene
Mzimu wa Mulungu unkandionetsera.

Kenaka masomphenya amene ndinkawaonawo anayamba kuzimirira.
25 Ndipo ndinafotokozera akapolowo zonse zimene Yehova anandionetsa.

# 12

### *Chifaniziro cha Otengedwa Ukapolo*

1 Yehova anayankhula nane kuti, 2 "Iwe mwana wa munthu, ukukhala
pakati pa anthu owukira, iwowo maso openyera ali nawo, koma sakuona

ndipo makutu omvera ali nawo, koma sakumva chifukwa choti ndi anthu
owukira.
3 “Choncho, iwe mwana wa munthu, longedza katundu wako wopita
naye ku ukapolo. Unyamuke nthawi yamasana iwo akuona. Uchite ngati
wanyamuka kuchoka kumene ukukhala kupita ku dziko lachilendo iwowo
akuona. Mwina adzamvetsetsa, paja ndi anthu aupandu. 4 Utulutse
katundu wako wopita naye ku ukapolo nthawi ya masana iwo akuona.
Ndipo nthawi ya madzulo, iwo akuona, uchoke monga ngati ukupita ku
ukapolo. 5 Iwo akuona, ubowole pa khoma ndipo utulutsirepo katundu
wako. 6 Usenze katundu wako pa phewa iwo akuona, ndipo upite kunja ku
mdima. Uphimbe nkhope yako kuti usaone pansi, pakuti ndakusandutsa
iwe chizindikiro chochenjeza Aisraeli.”
7 Choncho ine ndinachita monga momwe anandilamulira. Nthawi
yamasana ndinatulutsa zinthu zanga nditazimanga ngati ndikupita ku
ukapolo. Ndipo nthawi yamadzulo ndinabowola khoma ndi manja anga.
Pamene chisisira chinkayamba, ndinasenza katundu wanga pa phewa
kutuluka naye iwo akuona.
8 Mmawa mwake Yehova anandiyankhula nati: 9 “Iwe mwana wa
munthu, kodi anthu aupandu a Israeli sanakufunse kuti ukuchita chiyani?
10 “Uwawuze kuti, ‘zimene ndikunena Ine Ambuye Wamphamvuzonse
ndi izi: Uthengawu ndi wonena za kalonga wa ku Yerusalemu pamodzi
ndi banja lonse la Israeli amene akukhala kumeneko.’ 11 Uwawuze kuti,
‘Ndiwe chizindikiro chowachenjeza.’
“Zidzakuchitikirani monga momwe zakuchitikira iwemu. Iwo adza-
tengedwa kupita ku ukapolo.”
12 “Kalonga wawo adzatenga katundu wake n’chisisira n’kunyamuka.
Adzatulukira pa bowo limene anthu anabowola pa khoma. Adzaphimba
nkhope yake kuti asaone kumene akupita. 13 Ndidzayala ukonde wanga pa
iye ndi kumukola mu msampha wanga. Ndidzabwera naye ku Babuloni,
dziko la Akaldeya, koma sadzaliona dzikolo, ndipo adzafera kumeneko.
14 Ine ndidzabalalitsa kumbali zonse zinayi onse okhala naye pafupi,
ndiwo omuthandiza ake pamodzi ndi ankhondo ake. Ndidzawalondola
ndi lupanga losolola.
15 “Iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, ndikadzawamwaza pakati
pa anthu a mitundu ina ndi kuwabalalitsira ku mayiko ena. 16 Koma
ndidzasiyako ena pang’ono amene adzapulumuke ku lupanga, njala ndi
mliri, kuti akafotokoze ntchito zawo zonse zonyansa pakati pa anthu
achilendo kumene akupitako. Pamenepo adzadziwa kuti ndine Yehova.”
17 Pambuyo pake Yehova anandiyankhulanso nati, 18 “Iwe mwana wa
munthu, uzinjenjemera ukamadya chakudya chako, ndipo uzinthunthu-
mira ndi mantha ukamamwa madzi ako. 19 Uwawuze anthu a m’dzikomo
kuti izi ndi zimene Ambuye Wamphamvuzonse akunena za anthu okhala
mu Yerusalemu ndi dziko la Israeli: Iwo adzadya chakudya chawo ndi
mantha ndi kumwa madzi awo ndi nkhawa. Zonse za m’dziko lawo
zidzalandidwa chifukwa cha ziwawa za anthu onse okhala m’menemo.
20 Mizinda imene ili ndi anthu idzasakazika ndipo dziko lidzasanduka
chipululu. Pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.”
21 Yehova anayankhulanso nane kuti, 22 “Iwe mwana wa munthu, kodi
mwambi umene ukunenedwa mu Israeli ndi wotani: ‘Masiku akupita
koma masomphenya onse sakukwaniritsidwa?’ 23 Choncho uwawuze
anthuwo kuti, ‘Ine Ambuye Yehova ndidzawuthetsa mwambi umenewu
ndipo sadzawunenanso mu Israeli.’ Uwawuze kuti, ‘masiku ayandikira oti

zonse zimene ndinanena m'masomphenya zichitikedi. 24 Pakuti masiku
amenewo sikudzakhalanso masomphenya abodza kapena kuwombeza
kwa chinyengo pakati pa anthu a Israeli. 25 Koma Ine Ambuye ndidza-
yankhula chimene ndikufuna, ndipo chidzachitikadi, osachedwa ayi.
Pakuti m'masiku anu omwe ano, inu anthu opanduka, ndidzakwaniritsa
chilichonse chimene ndidzanena. Ndikutero Ine Yehova.' "
26 Yehova anandiyankhula nati: 27 "Iwe mwana wa munthu, Aisraeli
akunena kuti, 'masomphenya amene ukuona sadzachitika kwa zaka
zambiri. Iwo akuti ukulosa za zinthu zimene zidzachitika ku tsogolo
kwambiri.'
28 "Choncho uwawuze kuti, 'zimene Ine Ambuye Yehova ndikunena
ndi izi: Zonena zanga sizidzachedwanso; chilichonse chimene ndikunena
chidzachitikadi. Ndikutero Ine Yehova.' "

# 13

*Mawu Odzudzula Aneneri Onyenga*

1 Yehova anayankhulanso nane kuti, 2 "Iwe mwana wa munthu
unenere modzudzula aneneri a Israeli amene akunenera za kukhosi
kwawo. Uwawuze iwowa kuti, 'Imvani mawu a Yehova!' 3 Ambuye
Yehova akuti, 'Tsoka kwa aneneri opusa amene amangonenera zopeka
ngakhale kuti sanaone kanthu konse!' 4 Iwe Israeli, aneneri ako ali
ngati nkhandwe pa mabwinja. 5 Simunakwere khoma kuti mukakonze
m'mene munagumuka, kuti Aisraeli adziteteze kolimba pa nkhondo pa
tsiku la Yehova. 6 Masomphenya awo ndi achabe ndipo kuwombeza
kwawo ndi kwabodza. Iwo amati, 'Yehova akutero,' pomwe Yehova
sanawatume. Komabe iwo amayembekezera kuti zimene ayankhulazo
zichitikadi. 7 Koma Ine ndikuti masomphenya anu ngachabechabe ndi
zimene mwawombedzazo n'zabodza. Mumanena kuti, 'Akutero Yehova,'
pamene sindinayankhule n'komwe.
8 "Tsono Ine Ambuye Wamphamvuzonse ndikukutsutsani chifukwa cha
zoyankhula zanu zonama ndi masomphenya anu abodzawo. Ndikutero
Ine Yehova. 9 Ndidzalanga aneneri amene amanenera zabodza za zinthu
zimene amati anaziona m'masomphenya. Sadzakhala nawo m'bwalo la
anthu anga ndipo mayina awo sadzalembedwa mu kawundula wa nzika
za Israeli. Sadzalowa nawo m'dziko la Israeli. Pamenepo mudzadziwa
kuti Ine ndine Ambuye Yehova.
10 "Popeza kuti aneneri asocheretsa anthu anga pomanena kuti,
'Kuli mtendere' pamene mtendere palibe; ndiponso anthu akamanga
khoma iwo n'kumalipaka njereza, 11 choncho ufotokozere amene alipaka
njerezawo kuti khomalo lidzagwa. Mvula idzagwa mwamphamvu,
kudzagwa matalala akuluakulu, ndipo kudzawomba mphepo yamkuntho.
12 Pamene khomalo lagwa, kodi anthu sadzakufunsani kuti, 'Kodi njereza
yemwe munapaka uja ali kuti?'
13 "N'chifukwa chake Ambuye Yehova akuti: Mwa ukali ndidzakunthitsa
mphepo ya mkuntho. Ndidzagwetsa matalala akuluakulu ndili ndi ukali
ndipo ndidzavumbwitsa mvula yamphamvu ndi mkwiyo mpaka khomalo
litawonongeka kotheratu. 14 Ndidzagwetsa khoma limene munalipaka
njerezalo. Ndidzaligumuliratu mpaka pansi kotero kuti maziko ake
adzaoneka. Khomalo likadzagwa, inu mudzawonongekamo; ndipo
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 15 Kotero ndidzagwiritsa ntchito
mkwiyo wanga pa khomali ndi pa amene analipaka njereza. Pambuyo
pake ndidzakuwuzani kuti, 'Khoma lagwa pamodzi ndi amene analipaka

njereza. 16 Agwanso aneneri a Yerusalemu amene ankalosa za Yerusalemu
n'kumati anaona m'masomphenya za mtendere wa Yerusalemu pamene
mtendere kunalibe konse, akutero Ambuye Wamphamvuzonse.'

17 "Tsono iwe mwana wa munthu, yankhulapo pa nkhani za akazi
amene ali pakati pa anthu ako. Iwo amanenera zopeka za m'mutu
mwawo. Tsono adzudzule. 18 Uwawuze kuti, 'Ambuye Yehova akuti:
Tsoka kwa akazi amene amasoka zithumwa zapamkono, amenenso
amasoka nsalu za kumutu za anthu. Kodi mufuna kukola mitima ya anthu
anga, inuyo n'kupulumutsa moyo wanu? 19 Ponamiza anthu anga amene
amamva za mabodza anu, inu mwapha anthu amene sanayenera kufa
ndipo mwasiya ndi moyo amene sanayenera kukhala ndi moyo.

20 " 'N'chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ine ndikudana
ndi zithumwa zanu zimene mumakokera nazo mitima ya anthu ngati
mbalame. Ndidzazing'amba kudzichotsa pa mikono yanu. Choncho
ndidzapulumutsa miyoyo ya anthu amene munawakola ngati mbalame.
21 Ndidzang'amba nsalu zanu za matsengazo ndi kupulumutsa anthu anga
m'manja mwanu, ndipo simudzakhalanso ndi mphamvu yowakolera.
Pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 22 Popeza kuti
munatayitsa mtima anthu olungama ngakhale sindinafune kuti ataye
mtima; ndipo munalimbitsa anthu oyipa kuti asaleka machimo awo
motero sakutha kupulumutsa moyo wawo, 23 choncho inu simudzaonanso
masomphenya abodza kapena kuwombeza. Ine ndidzapulumutsa anthu
anga m'manja mwanu. Ndipo pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.' "

# 14

### *Yehova Adzudzula Opembedza Mafano*

1 Tsiku lina ena mwa akuluakulu a Israeli anabwera kwa ine ndipo
anakhala pansi pamaso panga. 2 Ndipo Yehova anandipatsa uthenga uwu
nati, 3 "Iwe mwana wa munthu, anthu awa ayika mtima pa mafano
awo. Ayikanso maso awo pa zinthu zina zoyipa zopunthwitsa. Kodi
ayembekezera kuti ndiwayankhe chimene atandifunse? 4 Tsono yankhula
nawo ndi kuwawuza kuti zimene akunena Ambuye Yehova: 'Ngati
Mwisraeli aliyense ayika mtima wake pa mafano ndi kuyika maso ake pa
zinthu zoyipa zopunthwitsa, kenaka n'kupita kwa mneneri, Ineyo Yehova
mwini wakene ndidzamuyankha molingana ndi kuchuluka kwa mafano
ake. 5 Ine ndidzachita zimenezi kuti mwina n'kukopa mitima ya anthu a
Israeli, amene andisiya chifukwa cha mafano awo.'

6 "N'chifukwa chake uwawuze Aisraeli kuti Ine Ambuye Yehova ndikuti:
Lapani! Siyani mafano anu ndi ntchito zanu zonse zonyansa!

7 " 'Ngati Mwisraeli wina aliyense kapena mlendo wina aliyense
wokhala pakati pa Israeli adzichotsa yekha kwa Ine ndi kuyika mtima
pa mafano ake ndi kuyikanso maso ake pa zinthu zopunthwitsa ndipo
kenaka n'kupita kwa mneneri kukafunsa nzeru, Ineyo Yehova mwini
wakene ndidzamuyankha. 8 Ine ndidzalimbana naye munthu ameneyo
ndipo ndidzamusandutsa chitsanzo ndi chisudzo. Ndidzamuchotsa pakati
pa anthu anga. Pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

9 " 'Ndipo ngati mneneri anyengedwa nanenera, Ine Yehova ndiye
ndamunyenga mneneri ameneyo, ndipo ndidzatambasula dzanja langa
kumukantha ndi kumuwononga pakati pa anthu anga Aisraeli. 10 Iwo

adzalangidwa chifukwa cha kulakwa kwawo. Chilango cha wodza-
funsira nzeru kwa mneneri chidzafanana ndi chilango cha mneneriyo.
11 Ndidzachita zimenezi kuti Aisraeli asasocherenso kundisiya Ine ndi kuti
asadziyipitsenso ndi machimo awo. Adzakhala anthu anga, ndipo Ine
ndidzakhala Mulungu wawo, akutero Ambuye Yehova.' "

### *Chilango Chosathawika*

12 Yehova anayankhula nane kuti, 13 "Iwe mwana wa munthu, ngati
dziko lindichimwira posandikhulupirira, Ine ndidzatambasula dzanja
langa kulikantha pochepetsa chakudya chake. Ndidzatumiza njala pa
dzikolo ndi kuwononga anthu ake ndi nyama zomwe. 14 Ngakhale anthu
atatu awa, Nowa, Danieli ndi Yobu akanakhala m'menemo, akanangop-
ulumutsa moyo wawo chifukwa cha chilungamo chawo. Ndikutero Ine
Ambuye Yehova.

15 "Kapena ndikanatumiza zirombo m'dziko monse ndi kulisiya lopanda
anthu, ndipo dzikolo n'kukhala chipululu chakuti munthu sangadutse
chifukwa cha zirombo. 16 Apanso, ndikunenetsa Ine Ambuye Yehova
kuti, 'Ngakhale anthu atatu awa akanakhalamo, sakanatha kupulumutsa
ana awo aamuna ndi aakazi. Iwo okha akanapulumuka, koma dziko
likanasanduka chipululu.'

17 "Kapena ndikanatumiza lupanga m'dzikolo ndi kunena kuti, 'Lupanga
lipite m'dziko monse,' ndi kuwononga anthu ake ndi nyama zomwe.
18 Apanso ndikunenetsa Ine Ambuye Yehova kuti, 'Ngakhale anthu atatu
awa akanakhalamo, sakanatha kupulumutsa ana awo aamuna kapena ana
aakazi. Iwo okha akanapulumuka.'

19 "Kapena ndikanatumiza mliri m'dzikomo ndi kuonetsa ukali wanga
pokhetsa magazi, kuwononga anthu ake ndi nyama zomwe. 20 Apanso
ndikunenetsa Ine Ambuye Yehova kuti ngakhale Nowa, Danieli ndi
Yobu akanakhala m'menemo, sakanatha ngakhale kupulumutsa mwana
wamwamuna kapena wamkazi. Akanangodzipulumutsa okha chifukwa
cha chilungamo chawo.

21 "Pakuti Ambuye Yehova akuti: Kudzakhala zoopsa kwambiri pamene
ndidzatumiza pa Yerusalemu zilango zanga zinayi izi: lupanga, njala,
zirombo ndi mliri kuti ziwononge anthu ake ndi nyama zomwe!
22 Komabe padzakhala ena opulumuka, ana aamuna ndi ana aakazi
amene adzatulutsidwa m'dzikomo. Iwo adzabwera kwa inu, ndipo
mukadzaona makhalidwe awo ndi zochita zawo, mitima yanu idzakhala
pansi mukadzakumbukira chilango chimene ndinachita pa Yerusalemu.
23 Mitima yanu idzakhala pansi mukadzaona makhalidwe awo ndi zochita
zawo. Tsono mudzadziwa kuti Yerusalemu sindinamuchite zimenezi
popanda chifukwa, akutero Ambuye Yehova."

## 15

### *Yerusalemu, Mtengo Wamphesa Wosabereka*

1 Yehova anayankhulanso nane kuti, 2 "Iwe mwana wa munthu, kodi
mtengo wamphesa umapambana bwanji mtengo wina uliwonse? Nthambi
zake zimapambana bwanji nthambi ina iliyonse. 3 Mtengo umene
uja n'kupangira chiyani? Kodi anthu angathe kupangira chikhomo
chokolekapo zinthu zawo? 4 Taonani, ndi nkhuni chabe zosonkhera
moto. Ukaponyedwa pa moto monga nkhuni ndi kuyaka mbali zonse
ndi kusanduka makala, kodi ungagwiritsidwe ntchito ina iliyonse? 5 Ngati

pamene unali wosapsa sukanatheka kuwugwiritsa ntchito, nanga bwanji utapserera ndi moto, adzawugwiritsa ntchito bwanji?
6 "N'chifukwa chake Ambuye Yehova akuti, 'Mtengo wamphesa ndidza-
wuponya m'moto monga ndimachitira ndi mitengo ina ya ku nkhalango.
Momwemonso ndidzachita ndi anthu a ku Yerusalemu. 7 Ndidzawalanga
pamenepo ngakhale iwo atuluka pa moto, motowo udzawatenthabe.
Ndipo pamene ndidzatsutsana nawo, mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.
8 Ine ndidzasandutsa dziko kukhala chipululu chifukwa anthu akhala
osakhulupirika, akutero Ambuye Yehova.' "

## 16

*Kusakhulupirika kwa Yerusalemu*

1 Yehova anayankhula nane kuti, 2 "Iwe mwana wa munthu, udzudzule
Yerusalemu za ntchito zake zonyansa. 3 Umuwuze kuti, 'Ambuye Yehova
akukuwuza, iwe Yerusalemu kuti: Kwawo kwa makolo ako ndi ku Kanaani ndipo iwe unabadwira komweko. Abambo ako anali Mwamori,
amayi ako anali Mhiti. 4 Pa tsiku lomwe unabadwa sanadule mchombo
wako. Sanakusambitse m'madzi kuti uyere. Sanakuthire mchere kapena
kukukulunga m'nsalu. 5 Palibe ndi mmodzi yemwe anakusamala kapena
kukumvera chisoni kuti akuchitire zimenezi. M'malo mwake anakutaya panja poyera, chifukwa ananyansidwa nawe pa tsiku lako lobadwa.
6 " 'Tsono pamene ndinkadutsa, ndinakuona ukuvimvinizika m'magazi
ako. Ndinakuyankhula uli m'magazi ako omwewo kuti, 'Khala ndi moyo,'
7 ndi kuti ukule ngati mbewu ya m'munda. Iwe unakula ndipo unatalika
ndi kutha msinkhu. Mawere ako anayamba kumera ndi tsitsi lakonso linayamba kutalika. Komabe unali wamaliseche ndi wausiwa.
8 " 'Tsono pamene ndinkadutsanso ndinaona kuti nthawi yako yomanga
banja inakwana. Tsono ndinakufunditsa chovala changa ndi kubisa umaliseche wako. Ndinachita nawe pangano la ukwati ndipo unakhala wanga, akutero Ambuye Wamphamvuzonse.
9 " 'Ine ndinakusambitsa m'madzi kutsuka magazi ako ndikukud-
zoza mafuta. 10 Ndinakuveka zovala zopetapeta ndi nsapato za
chikopa. Ndinakuveka zovala zabafuta ndi kukuveka zovala za bafuta.
11 Ndinakukongoletsa ndi zokometsera zamtengowapatali: ndinakuveka
zibangiri m'manja mwako ndi mkanda m'khosi mwako, 12 ndipo ndinaku-
veka chipini pa mphuno yako, ndolo ku makutu ako ndiponso chipewa
chaufumu pa mutu wako. 13 Choncho unavala zokongoletsa zagolide
ndi siliva. Zovala zako zinali zabafuta, zasilika ndi za nsalu zopetapeta. Chakudya chako chinali ufa wosalala uchi ndi mafuta a olivi. Motero
unakhala wokongola kwambiri ndipo unasanduka mfumukazi. 14 Ndipo
mbiri ya kukongola kwako inawanda pakati pa anthu a mitundu ina, chifukwa ulemerero umene ndinakupatsa unapititsa patsogolo kukongola kwako, akutero Ambuye Yehova.
15 " 'Koma iwe unatama kukongola kwako ndipo unayamba kuchita
zadama chifukwa cha kutchuka kwako. Unkachita chigololo ndi kumangodzipereka kwa aliyense wodutsa ndipo kukongola kwako kunakhala
kwake. 16 Unatenga zovala zako zina nukakongoletsera malo opem-
bedzerako mafano, ndipo kumeneko umachitirako zigololo. Zinthu
izi sizinachitikepo n'kale lomwe ndipo sizidzachitikanso. 17 Unatenga
zokongoletsera zopangidwa ndi golide ndi siliva zimene ndinakupatsa

ndipo unadzipangira wekha mafano aamuna amene unkachita nawo za
dama. 18 Ndipo iwe unatenga zovala zako zopetapeta ndi kuveka mafano.
Mafuta anga ndi lubani wanga unapereka kwa mafanowo. 19 Chakudya
chimene ndinakupatsa, ufa, mafuta ndi uchi, zimene ndinkakudyetsa nazo
unazitenga n'kuzipereka kwa mafanowo ngati nsembe ya fungo lokoma.
Ndikutero Ine Ambuye Yehova.

20 " 'Ndipo unatenga ana ako aamuna ndi ana aakazi amene
unandibalira ine, ndipo unakawapereka ngati nsembe kwa mafanowo.
Kodi zigololo zakozo sizinakukwanire 21 kuti uziphanso ana anga ndi
kuwapereka ngati nsembe kwa mafano akowo? 22 Chifukwa cha zadama
zako zonyansazi unayiwala masiku a ubwana wako pamene unali wa-
maliseche, wausiwa ndiponso womangovivinizika m'magazi.

23 " 'Tsoka! Tsoka kwa iwe, akutero Ambuye Yehova chifukwa powon-
jezera pa zoyipa zako zonse, 24 wadzimangira wekha nsanja ndi guwa
pa mabwalo onse. 25 Pa msewu uliwonse wamanga nsanjazo. Motero
wanyazitsa kukongola kwako podzipereka kwa aliyense amene adutsapo.
26 Umachita chigololo ndi Aigupto, anthu adama oyandikana nawe. Chon-
cho unandikwiyitsa chifukwa unachulukitsa za dama zako. 27 N'chifukwa
chake ndinatambasula dzanja langa kukukantha ndi kuchepetsa dziko
lako. Ndinakupereka kwa adani ako, Afilisti amene amayipidwa ndi
makhalidwe ako onyansa. 28 Chifukwa cha chilakolako chako unachitanso
zadama ndi Aasiriya. Ngakhale unachita nawo chigololo koma sunakhutit-
sidwebe. 29 Choncho unapitirirabe kuchita chigololo ndi Ababuloni,
anthu a m'dziko lokonda zamalonda. Ngakhale unachita izi, komabe
sunakhutitsidwe.

30 " 'Ambuye Yehova akuti: Mtima wako ndi wofowoka kwambiri
chifukwa unachita zonsezo monga ngati mkazi wopanga manyazi.
31 Unamanga nsanja pa msewu uliwonse. Unamanganso kachisi pabwalo
lililonse. Komabe sunachite ngati mkazi wadama chifukwa unakana
malipiro.

32 " 'Iwe mkazi wachigololo! Umakonda amuna achilendo kupambana
mwamuna wakowako! 33 Amuna ndiwo amapereka malipiro kwa mkazi
wadama. Koma iwe ndi amene ukupereka mphatso kwa zibwenzi zako
zonse. Choncho umazinyengerera kuti zizibwera kwa iwe kuchokera
mbali zonse kudzagona nawe. 34 Chotero iwe ukusiyana ndi akazi
ena achigololo, pakuti palibe amene ankakunyengerera kuti uchite naye
chigololo. Iweyo ndiye unkapereka ndalama osati ena kukupatsa ndalama
ayi. Motero unalidi wosiyana kwambiri ndi akazi ena.

35 " 'Tsono mkazi wachigololo iwe, imva mawu a Yehova! 36 Ambuye
Yehova akuti, popeza unavula ndi kuonetsa umaliseche wako mopanda
manyazi, unachita chigololo ndi zibwenzi zako pamodzi ndi mafano ako
onyansa, komanso popeza unapereka ana ako kuti aphedwe ngati nsembe
zoperekedwa kwa mafano, 37 n'chifukwa chake Ine ndidzasonkhanitsa
zibwenzi zako zonse, zimene unkasangalala nazo, amene unkawakonda
ndi amene unkawada. Ndidzawasonkhanitsa motsutsana nawe kuchokera
ku madera onse okuzungulira ndipo Ine ndidzakuvula pamaso pawo,
ndipo iwo adzaona umaliseche wako wonse. 38 Ine ndidzakulanga monga
mmene amalangira akazi amene amachita chigololo ndiponso opha anthu.
Chifukwa cha ukali wanga ndi nsanje yanga, ndidzakhetsa magazi ako
mokwiya kwambiri. 39 Ndidzakupereka m'manja mwa zibwenzi zako ndi
kuwononga nyumba zopembedzera mafano ako. Iwo adzakuvula zovala

zako ndi kutenga zodzikometsera zako zabwino. Choncho adzakusiya wa
maliseche ndi wausiwa. 40 Iwo adzabweretsa gulu la anthu limene lidza-
kuponya miyala ndi kukutematema ndi malupanga awo. 41 Adzatentha
nyumba zako ndi kukulanga iwe pamaso pa akazi ambiri. Ndidzathetsa
chigololo chako, ndipo sudzalipiranso zibwenzi zako. 42 Ukali wanga
udzalekera pamenepo ndipo sindidzakuchitiranso nsanje. Ndidzakhala
chete osakwiyanso.

43 " 'Popeza sunakumbukire masiku a ubwana wako koma unandikwiy-
itsa ndi zinthu zonsezi, Ine ndidzakubwezera ndithu chilango pamutu
pako chifukwa cha zimene wachita, akutero Ambuye Yehova. Paja
unawonjezera chigololo pa machitidwe ako onyansa.

44 " 'Taona, onse onena miyambi adzakuphera mwambi wakuti, 'Make
mbuu, mwana mbuu.' 45 Ndiwedi mwana weniweni wamkazi wa mayi
wako, amene amanyoza mwamuna wake ndi ana ake. Ndiwe m'bale
weniweni wa abale ako, amene amanyoza amuna awo ndi ana awo. Amayi
ako anali Mhiti ndipo abambo ako anali Mwamori. 46 Mkulu wako anali
Samariya, ndipo iye pamodzi ndi ana ake aakazi ankakhala cha kumpoto
kwako. Mng'ono wako, Sodomu ankakhala cha kummwera kwako
pamodzi ndi ana ake aakazi. 47 Iwe sunangotsatira kokha njira zawo
zoyipa ndi kuchita zonyansa zawo, koma patangopita nthawi pang'ono
machitidwe ako oyipa anaposa awo. 48 Ndithu pali Ine wamoyo, akutero
Ambuye Yehova, ngakhale m'bale wako Sodomu ndi ana ake aakazi
sanachitepo zimene iwe ndi ana ako aakazi munachita.

49 " 'Tsono tchimo la m'bale wako Sodomu linali ili: Iye ndi ana ake
aakazi ankanyadira kuchuluka kwa chakudya ndi chuma chawo. Koma
sanalabadireko kuthandiza osauka ndi aumphawi. 50 Anali odzitukumula
ndipo ankachita zonyansa pamaso panga. N'chifukwa chake ndinawa-
chotsa monga mmene waoneramu. 51 Samariya sanachite ngakhale theka
la machimo amene unachita. Iwe wachita zinthu zonyansa zambiri
kuposa iwo, motero kuti abale ako awiriwo amaoneka ngati olungama
kuyerekeza ndi iye. 52 Tsono iwenso uyenera kuchita manyazi popeza
waonetsa abale ako ngati osachimwa. Popeza kuti machimo ako ndi
onyansa kwambiri kupambana awo, tsonotu iwowo akuoneka olungama
kupambana iweyo. Choncho iwenso uchite manyazi ndi kunyozedwa
popeza unaonetsa abale ako ngati olungama.

53 " 'Koma, ndidzadalitsanso Sodomu ndi ana ake aakazi. Ndidzadal-
itsanso Samariya ndi ana ake aakazi. Pa nthawi yomweyo ndidza-
kudalitsanso iwe Yerusalemu. 54 Ndidzatero kuti uchite manyazi ndi
kunyozeka chifukwa cha zonse zimene unachita powatonthoza anthuwa.
55 Motero m'bale wako Sodomu ndi ana ake akadzakhala monga mmene
analili poyamba paja, ndiponso m'bale wako Samariya akadzakhalanso
monga mmene anali poyamba paja, ndiye kuti iwenso ndi ana ako
mudzakhala monga mmene munalili payamba paja. 56 Kale lija pamene
unkanyada, suja unkanyogodola m'bale wako Sodomu 57 kuyipa kwako
kusanadziwike? Koma tsopano wafanana naye. Wasandukano chinthu
chonyozeka kwa anthu a ku Edomu ndi kwa onse owazungulira ndiponso
kwa Afilisti. Ndithu onse amene akuzungulira amakunyoza. 58 Choncho
udzalangidwa chifukwa cha zigololo zako ndi machitidwe anu onyansa,
akutero Yehova.

59 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ndidzakulanga molingana ndi
zimene unachita. Iwe unanyoza lumbiro lako pophwanya pangano

langa. 60 Komabe, Ine ndidzakumbukira pangano limene ndinachita
nawe m'masiku a unyamata wako, ndipo ndidzakhazikitsa pangano
losatha ndi iwe. 61 Tsono udzakumbukira njira zako zakale. Udza-
chita manyazi polandiranso abale ako, wamkulu ndi wamng'ono
yemwe. Ndidzawaperekanso kwa iwe kuti akhale ngati ana ako
ngakhale kuti sali a m'pangano langa ndi iwe. 62 Kotero ndidzak-
hazikitsa pangano langa ndi iwe, ndipo iwe udzadziwa kuti Ine ndine
Yehova. 63 Ndikadzakukhululukira zoyipa zako zonse zimene unachita,
udzazikumbukira ndipo udzachita manyazi kwambiri, kotero kuti sudza-
tha n'kuyankhula komwe, akutero Ambuye Yehova.' "

# 17

## *Fanizo la Ziwombankhanga Ziwiri ndi Mtengo Wamphesa*

1 Yehova anayankhula nane kuti, 2 "Iwe mwana wa munthu, aphere
mwambi anthu a Israeli ndi kuwawuza fanizo. 3 Uwawuze kuti
Ambuye Yehova akuti, chiwombankhanga chachikulu, cha mapiko
amphamvu, nthenga zitalizitali zamathothomathotho chinabwera ku
Lebanoni. Chinagwira nthambi ya pamwamba pa mtengo wa mkungudza.
4 Chinabudula msonga yeniyeni ya nthambiyo n'kupita nayo ku dziko
lamalonda ndipo anakayika mu mzinda wa anthu amalonda.

5 " 'Kenaka chinatenga mbewu ina ya m'dziko ndi kukayidzala ku
malo a chonde kumene kunali madzi ambiri. Anayidzala ngati mmene
amadzalira mtengo wa msondozi. 6 Ndipo inaphuka nisanduka mtengo
wa mpesa wotambalala cham'munsi. Nthambi zake zinaloza mmwamba
kumene kunali chiwombankhangacho, koma mizu yake inalowa pansi.
Kotero unakhala mtengo wamphesa ndipo unasanduka wa nthambi
ndiponso wa masamba ambiri.

7 " 'Koma panali chiwombankhanga chinanso chachikulu, cha mapiko
amphamvu ndi cha nthenga zambiri. Tsopano mtengo wamphesa uja
unakhotetsera mizu yake kwa chiwombankhangacho kuchokera pa malo
amene unadzalidwa ndipo unatambalitsa nthambi zake kwa chiwom-
bankhangacho kufuna kuthiridwa madzi. 8 Koma mtengowo unadzalidwa
kale pa nthaka yabwino m'mbali mwa madzi kuti ukhale ndi nthambi
zambiri, ubereke zipatso ndi kukhala wokongola.'

9 "Ukawawuze Aisraeli kuti, 'Ambuye Wamphamvuzonse akuti: Kodi
udzakula bwino? Kodi chiwombankhanga chija sichidzawuzula mizu
ndi kubudula nthambi zake kuti ufote? Masamba ake onse anthete
adzafota. Sipadzafunika dzanja lamphamvu kapena anthu ambiri kuti
awuzule. 10 Ngakhale utawokedwa pena, kodi udzaphuka? Kodi
sudzafoteratu mphepo ya kummawa ikadzawomba, kufotera pa malo
pamene anawuwokerapo?' "

11 Kenaka Yehova anandiyankhula nati: 12 "Tawafunsa anthu owuki-
rawa kuti, 'kodi mukudziwa tanthauzo la zinthu zimenezi?' Uwafo-
tokozere kuti, 'Mfumu ya Babuloni inapita ku Yerusalemu ndikukatengako
mfumu ndi anthu ake otchuka ndi kubwera nawo ku Babuloni. 13 Ndipo
anatenga mmodzi wa banja laufumu ndi kuchita naye mgwirizano,
ndipo anamulumbiritsa kuti akhale womvera. Inatenganso akulu onse a
m'dzikomo 14 kuti ufumu wa dzikolo utsitsidwe, usadzaphukenso, koma
kuti ukhalepobe posunga pangano limene unachita. 15 Koma mfumu
inawukira mfumu ya ku Babuloni potumiza nthumwi ku dziko la Igupto
kukatenga akavalo ndi gulu lalikulu la nkhondo. Kodi mfumu yotereyi

ingapambane? Kodi wochita zinthu zoterezi angapulumuke? Kodi
angaphwanye mgwirizano ndi kupulumuka?
16 “ ‘Ndithu pali Ine wamoyo, akutero Ambuye Yehova, mfumuyo
idzafera ku Babuloni, m’dziko la mfumu imene inayika pa mpando wau-
fumu. Inapeputsa lumbiro lake n’kuphwanya pangano limene inachita
ndi mfumu inayo. 17 Farao ndi gulu lake lankhondo lamphamvu sadzatha
kumuthandiza pa nkhondo, pamene mfumu ya Babuloni idzapanga
mitumbira ya nkhondo ndi nsanja za nkhondo kuti iwononge miyoyo
yambiri. 18 Mfumu ya ku Yuda inanyoza lumbiro lake pophwanya
pangano. Inalonjeza komabe sinatsatire malonjezo ake. Choncho
sidzapulumuka.
19 “ ‘N’chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ndithu pali Ine
wamoyo, Ine ndidzalanga mfumu imeneyi chifukwa inanyoza lumbiro
langa, ndi kuphwanya pangano langa. 20 Ndidzayitchera ukonde ndipo
idzakodwa mu msampha wanga. Ndidzapita nayo ku Babuloni ndi
kuyilanga kumeneko chifukwa inali yosakhulupirika kwa Ine. 21 Asilikali
ake onse amene akuthawa adzaphedwa ndi lupanga, ndipo opulumuka
adzabalalitsidwa ku mbali zonse. Ndipo iwo adzadziwa kuti Ine Yehova
ndayankhula.
22 “ ‘Ambuye Yehova akuti: Ine mwini ndidzatenga nthambi pamwamba
penipeni pa mkungudza ndi kuyidzala; ndidzathyola nthambi yanthete
kuchokera pa nthambi zapamwamba penipeni ndi kuyidzala pamwamba
pa phiri lalitali. 23 Ndidzayidzaladi pa phiri lalitali la Israeli. Idza-
phuka nthambi ndi kubereka zipatso. Choncho idzasanduka mkungudza
wamphamvu. Mbalame za mtundu uliwonse zidzamanga zisa zawo
m’menemo; zidzapeza malo okhala mu mthunzi wa nthambi zake.
24 Mitengo yonse yakuthengo idzadziwa kuti Ine ndine Yehova amene
ndimafupikitsa mitengo yayitali ndi kutalikitsa mitengo yayifupi. Ndi-
mawumitsa mitengo yabiriwiri ndi kubiriwitsa mitengo yowuma.
“ ‘Ine Yehova ndayankhula zimenezi, ndipo ndidzazichita.’ ”

# 18

*Munthu Wochimwa Adzafa*

1 Yehova anandiyankhula nati: 2 “Kodi anthu inu mumatanthauza
chiyani mukamabwerezabwereza kunena mwambi uwu wokhudza dziko
la Israeli kuti:
“ ‘Nkhuyu zodya akulu zimapota
ndi ana omwe?’ ”
3 “Ndithu pali Ine wamoyo, akutero Ambuye Yehova, simudzanenanso
mwambi umenewu mu Israeli. 4 Pakuti moyo uliwonse ndi wanga. Moyo
wa abambo ndi wanga, wamwananso ndi wanga. Munthu wochimwa ndi
amene adzafe.
5 “Tiyerekeze kuti pali munthu wolungama
amene amachita zolungama ndi zolondola.
6 Iye sadyera nawo pa mapiri a chipembedzo
kapena kupembedza mafano a Aisraeli.
Iye sayipitsa mkazi wa mnzake
kapena kugonana ndi mkazi pamene akusamba.
7 Iye sapondereza munthu wina aliyense,
koma amabwezera wangongole n’chigwiriro chake.
Iye salanda zinthu za osauka,

koma amapereka chakudya kwa anthu anjala,
ndipo amapereka zovala kwa anthu ausiwa.
8 Iye sakongoletsa ndalama mwa katapira,
kapena kulandira chiwongoladzanja chachikulu.
Amadziletsa kuchita zoyipa
ndipo sakondera poweruza milandu.
9 Iye amatsatira malangizo anga,
ndipo amasunga malamulo anga mokhulupirika.
Munthu ameneyo ndi wolungama;
iye adzakhala ndithu ndi moyo,
akutero Ambuye Yehova.

10 “Tiyerekeze kuti munthu wolungama chotere wabala mwana chim-
balangondo amene amakhalira kupha anthu ndi kuchita zinthu zina
zotere. 11 Iye n’kumachita zinthu zimene ngakhale abambo ake sana-
chitepo.
“Amadyera nawo ku mapiri achipembedzo.
Amayipitsa mkazi wa mnzake.
12 Iye amapondereza munthu wosauka ndi wosowa.
Amalanda zinthu za osauka.
Sabweza chikole cha munthu wa ngongole.
Iye amatembenukira ku mafano
nachita zonyansa.
13 Iye amakongoletsa mwa katapira ndipo amalandira chiwongoladzanja
chachikulu.
Kodi munthu wotereyu n’kukhala ndi moyo? Ayi ndithu! Chifukwa
wachita zinthu zonyansa zonsezi, adzaphedwa ndipo adzalandira chilango
chomuyenera.

14 “Tsono tiyerekeze kuti munthu woyipa uyu wabala mwana amene
amaona machimo onse amene abambo ake ankachita. Ngakhale amaona
koma osatsanzira ntchito zake zoyipazo.
15 “Sadyera nawo pa mapiri achipembedzo.
Sapembedza mafano a ku Israeli.
Sayipitsa mkazi wa mnzake.
16 Sapondereza munthu wina aliyense.
Satenga chikole akabwereketsa chinthu. Salanda zinthu za osauka.
Salanda zinthu za munthu.
Amapereka chakudya kwa anthu anjala.
Amapereka zovala kwa anthu aumphawi.
17 Amadziletsa kuchita zoyipa.
Sakongoletsa kuti apezepo phindu. Salandira chiwongoladzanja.
Amasunga malangizo anga ndi kumvera malamulo anga.
Munthu wotereyo sadzafa chifukwa cha machimo a abambo ake. Adza-
khala ndi moyo ndithu. 18 Koma abambo ake, popeza kuti anazunza anthu
ena ndi kubera m’bale wawo ndiponso popeza kuti sanachitire zabwino
anansi ake, adzafera machimo ake omwe.

19 “Mwina inu mukhoza kufunsa kuti, ‘N’chifukwa chiyani mwana
salangidwa chifukwa cha kulakwa kwa abambo ake? Ayi, mwanayo
adzakhala ndi moyo chifukwa ankachita zolungama ndi zolondola ndipo
ankasamala kumvera malamulo anga onse. 20 Munthu wochimwa ndiye
amene adzafe. Mwana sadzapezeka wolakwa chifukwa cha abambo
ake, kapena abambo kupezeka wolakwa chifukwa cha mwana wawo.

Chilungamo cha munthu wolungama ndicho chidzamupulutse, ndipo kuyipa kwa munthu wochimwa ndiko kudzamuwonongetse.
21 " 'Munthu woyipa akatembenuka mtima ndi kusiya machimo amene ankachita ndi kuyamba kumvera malamulo anga ndi kumachita zol-
ungama ndi zokhulupirika, ndiye kuti adzakhala ndi moyo. Sadzafa ayi.
22 Zoyipa zake zonse zidzakhululukidwa. Chifukwa cha zinthu zolungama
zimene anazichita adzakhala ndi moyo. 23 Kodi Ine ndimakondwera
ndi imfa ya munthu woyipa? Ayi, ndimakondwera pamene woyipa watembenuka mtima kuti akhale ndi moyo. Akutero Ambuye Yehova.
24 " 'Koma ngati munthu wolungama apatuka kusiya zachilungamo ndi kuyamba kuchita tchimo ndi zonyansa za mtundu uliwonse zimene amachita anthu oyipa, kodi munthu wotereyu n'kukhala ndi moyo? Ayi ndithu, zolungama zake zonse sizidzakumbukiridwa. Iye adzayenera kufa chifukwa cha machimo amene anachita.
25 "Komabe inu mukunena kuti, 'Zimene Ambuye amachita ndi zopanda chilungamo.' Tamvani tsono inu Aisraeli: Kodi zochita zanga ndizo
zosalungama? Kodi si zochita zanu zimene ndi zosalungama? 26 Ngati
munthu wolungama atembenuka kusiya chilungamo chake ndi kuchita
tchimo, iye adzafa chifukwa cha tchimolo. 27 Koma ngati munthu woyipa
aleka zoyipa zake zimene anazichita ndi kuyamba kuchita zimene ndi
zolungama ndi zolondola, iye adzapulumutsa moyo wake. 28 Popeza
waganizira za zolakwa zonse ankachita ndipo wazileka, iye adzakhala ndi
moyo ndithu; sadzafa. 29 Komabe Aisraeli akunena kuti, 'Zimene Ambuye amachita ndi zopanda chilungamo.' Kodi zochita zanga ndizo zopanda chilungamo, inu Aisraeli? Kodi si zochita zanu zimene ndi zopanda chilungamo?
30 "Chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: inu Aisraeli, Ine ndidzakuweruzani aliyense wa inu molingana ndi ntchito zake. Lapani!
Lekani zoyipa zanu kuti musawonongeke nazo. 31 Tayani zolakwa
zanu zonse zimene munandichimwira nazo ndipo khalani ndi mtima
watsopano ndi mzimu watsopano. Kodi muferanji inu Aisraeli? 32 Ine
sindikondwera ndi imfa ya munthu aliyense, akutero Ambuye Yehova. Chifukwa chake, lapani kuti mukhale ndi moyo."

# 19

*Nyimbo ya Maliro a Akalonga a Israeli*

1 "Imba nyimbo ya madandawulo, kuyimbira akalonga a ku Israeli.
2 Uzinena kuti,
" 'Amayi ako anali ndani?
Anali ngati mkango waukazi!
Iwo unabwatama pakati pa mikango yayimuna;
unkalera ana ake pakati pa misona.
3 Unalera mmodzi mwa ana ake,
ndipo mwanayo anasanduka mkango wamphamvu.
Unaphunzira kugwira nyama,
ndipo unayamba kudya anthu.
4 Anthu amitundu anamva za mkangowo,
ndipo tsiku lina unagwa m'mbuna mwawo.
Iwo anawukoka ndi ngowe
kupita nawo ku dziko la Igupto.

5 “ ‘Amayi aja ataona kuti mwana ankamukhulupirira uja wagwidwa ndi
kuti chiyembekezo chake chapita padera,
amayiwo anatenganso mwana wina
namusandutsa mkango wamphamvu.
6 Unkayendayenda pakati pa mikango inzake,
pakuti tsopano unali mkango wamphamvu.
Unaphunzira kugwira nyama
ndipo unayamba kudya anthu.
7 Unagwetsa malinga awo,
ndikuwononga mizinda yawo.
Onse a m’dzikomo
anachita mantha chifukwa cha kubangula kwake.
8 Pamenepo mitundu ya anthu, makamaka ochokera madera ozungulira,
inabwera kudzalimbana nawo.
Anawutchera ukonde wawo,
ndipo tsiku lina unagwera m’mbuna mwawo.
9 Anawukoka ndi ngowe nawuponya m’chitatanga.
Anabwera nawo kwa mfumu ya ku Babuloni
ndipo mfumuyo inawuponya m’ndende
ndi cholinga choti liwu lake lisamamvekenso
ku mapiri a Israeli.

10 “ ‘Amayi ako anali ngati mpesa m’munda wamphesa
wodzalidwa m’mbali mwa madzi.
Unabereka bwino ndipo unali ndi nthambi zambiri
chifukwa cha kuchuluka kwa madzi.
11 Nthambi zake zinali zolimba,
zoyenera kupangira ndodo yaufumu.
Unatalika nusomphoka pakati pa
zomera zina.
Unkaoneka bwino chifukwa cha kutalika kwake,
ndi nthambi zake zambiri.
12 Koma unazulidwa mwaukali
ndipo unagwetsedwa pansi.
Unawuma ndi mphepo ya kummawa,
zipatso zake zinayoyoka;
nthambi zake zolimba zinafota
ndipo moto unapsereza mtengo wonse.
13 Ndipo tsopano anawuwokeranso ku chipululu,
dziko lowuma ndi lopanda madzi.
14 Moto unatulukanso mu mtengomo
ndi kupsereza nthambi ndi zipatso zake.
Palibe nthambi yolimba inatsala pa mtengowo
yoyenera kupangira ndodo yaufumu.
Imeneyi ndi nyimbo yachisoni ndipo yasanduka nyimbo ya pa maliro.’ ”

# 20

*Kuwukira kwa Israeli*

1 Tsiku lakhumi la mwezi wachisanu, chaka chachisanu ndi chiwiri, ena mwa akuluakulu a Israeli anabwera kudzapempha nzeru kwa Yehova, ndipo anakhala pansi pamaso panga.

2 Tsono Yehova anandiyankhula nati: 3 “Iwe mwana wa munthu,
ayankhule akuluakulu a Israeli ndi kuwawuza kuti, ‘Ambuye Yehova akuti:
Kodi mwabwera kudzapempha nzeru kwa Ine? Ndithu pali Ine wamoyo,
Ine sindidzakulolani kupempha nzeru kwa Ine, akutero Ambuye Yehova.’
4 “Kodi uwaweruza? Iwe mwana wa munthu, kodi ugamula mlandu
wawo? Uwadziwitse tsono zonyansa zimene anachita makolo awo,
uwawuze kuti, 5 ‘Ambuye Yehova akuti: Pa tsiku limene ndinasankha
Israeli, ndinalumbira kwa zidzukulu za nyumba ya Yakobo ndipo ndi-
nadziwulula kwa iwo ku Igupto. Ndinalumbira ndi kuwawuza kuti: Ine
ndine Yehova Mulungu wanu. 6 Pa tsiku limenelo ndinalumbira kwa
iwo kuti ndidzawatulutsa m’dziko la Igupto ndi kupita nawo ku dziko
limene ndinawapezera, dziko la mwana alirenji, dziko lokongola kwambiri
kupambana mayiko ena. 7 Ndipo ndinawawuza kuti, ‘Aliyense ataye
zinthu zonse zonyansa zimene ankasangalala nazo, ndipo musadziyipitse
ndi mafano a Igupto, Ine ndine Yehova Mulungu wanu.’
8 “ ‘Koma iwo anandiwukira ndipo sanafune kundimvera. Palibe amene
anataya zonyansa zonse zimene ankasangalala nazo. Panalibenso amene
anasiya mafano a ku Igupto. Tsono ndinaganiza zowakhuthulira ukali
wanga ndi kuwaonetsa mkwiyo wanga m’dziko la Igupto momwemo.
9 Koma sindinachite zimenezi chifukwa cha dzina langa, kuti lisayipit-
sidwe pakati pa anthu a mitundu ina amene ankakhala pakati pawo.
Paja ndinali nditaonetsa mphamvu zanga pamaso pa mitunduyo potulutsa
Aisraeli m’dziko la Igupto. 10 Choncho ndinawatulutsa m’dziko la
Igupto ndi kubwera nawo m’chipululu. 11 Ndinawapatsa malangizo anga
ndi kuwadziwitsa malamulo anga amene munthu aliyense akawamvera
adzakhala ndi moyo. 12 Ndinawapatsanso Masabata ngati chizindikiro
pakati pathu, kuti adziwe kuti Ine Yehova ndinawapatula.
13 “ ‘Komabe anthu a Israeli anandiwukira m’chipululu. Iwo sanat-
satire malangizo anga koma anakana malamulo anga amene munthu
aliyense akawamvera adzakhala ndi moyo. Ndipo anayipitsa kotheratu
Masabata anga. Choncho, ndinaganiza zowakhuthulira ukali wanga ndi
kuwawononga m’chipululu. 14 Koma sindinachite zimenezi chifukwa cha
dzina langa, kuti lisayipitsidwe pakati pa anthu a mitundu ina amene
anandiona ndikutulutsa Aisraeliwo mu Igupto. 15 Ndinalumbiranso kwa
iwo m’chipululu muja, nditakweza dzanja, kuti sindidzawalowetsanso
m’dziko limene ndinawapatsa, dziko la mwana alirenji, lokoma kwambiri
kuposa mayiko ena onse. 16 Paja anakana malamulo anga, sanatsatire
malangizo anga ndipo anayipitsa masabata anga. Mitima yawo inakonda
mafano. 17 Komabe ndinawamvera chisoni ndipo sindinawawononge
kapena kuwatheratu m’chipululu. 18 Tsono kwa ana awo m’chipululu ndi-
nati, ‘Musatsatire malangizo a makolo anu kapena kusunga malamulo awo
kapena kudziyipitsa ndi mafano awo. 19 Ine ndine Yehova Mulungu wanu;
tsatirani malangizo anga ndipo sungani malamulo anga. 20 Masabata anga
muziwasunga ngati opatulika kuti akhale chizindikiro pakati pa Ine ndi
inu. Mukatero mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu.’
21 “ ‘Koma ana awo anandiwukira. Iwo sanatsatire malangizo anga,
sanamvere malamulo anga, ngakhale kuti amapereka moyo kwa munthu
amene amawamvera. Ndiponso anayipitsa Masabata anga. Chon-
cho ndinaganiza zowakhuthulira ukali wanga ndi kuwawonongeratu
m’chipululu momwemo. 22 Koma sindinatero chifukwa cha dzina langa
kuti lisayipitsidwe pakati pa anthu a mitundu ina amene anandiona ndiku-
tulutsa Aisraeliwo mu Iguptomo. 23 Choncho ndinalumbira m’chipululu,

nditakweza dzanja langa, kuti ndidzawabalalitsa pakati pa anthu a
mitundu ina ndi kuwamwazira ku mayiko akutali, 24 chifukwa sanamvere
malamulo anga, anakana malangizo anga, nayipitsa masabata anga, ndi
kupembedza mafano a makolo awo. 25 Ine ndinawapatsanso malangizo
amene sanali abwino ndi malamulo amene sakanatha kupeza nawo moyo.
26 Ndinawalekerera kuti adziyipitse ndi mphatso zawo zomwe, makamaka
popereka ana awo oyamba kubadwa ngati nsembe zopsereza. Ndinatero
kuti ndiwadetse nkhawa ndi kuti adziwe kuti Ine ndine Yehova.’
27 “Tsono iwe mwana wa munthu, yankhula nawo Aisraeli ndipo
uwawuze kuti, ‘Ambuye Yehova akuti makolo anu anandinyozanso
posaonetsa moyo wokhulupirika. 28 Nditawalowetsa m’dziko limene
ndinachita kulumbirira kuti ndidzawapatsa, iwo tsono ankapita kulikonse
kumene anaona chitunda chachitali ndi mtengo wa masamba ambiri
kukapereka kumeneko nsembe ndi zopereka zawo zimene zinkandikwiy-
itsa. Kumeneko ankapereka nsembe za fungo lokoma ndiponso nsembe
za zakumwa. 29 Tsono ndinawafunsa kuti: Kodi chitunda chimene
mukupitako n’chotani? Chitundachi chakhala chikutchedwa mpaka lero
kuti ‘Chitunda cha Chipembedzo.’

### *Chiweruzo ndi Kubwezeretsa*

30 “Tsono uwawuze Aisraeli kuti, ‘Ine Ambuye Yehova ndikuti: Kodi
mudzadziyipitsa nokha monga anachitira makolo anu ndi kuchita
chigololo ndi milungu yawo yonyansa? 31 Pamene mubwera kudzapereka
mphatso zanu ndi kudzapereka ana kuti akhale ngati nsembe zopsereza
mumadziyipitsa ndi mafano anu mpaka lero. Kodi Aisraeli, ndingathe
kukulolani bwanji kuti mulandire malangizo kwa Ine? Ndithu pali Ine
wamoyo, akutero Ambuye Yehova, sindidzalola kuti mupemphe nzeru
kwa Ine.
32 “ ‘Inu munanena kuti, ‘Tikufuna tikhale ngati anthu a mitundu ina,
ngati anthu adziko lapansi, amene amapembedza mtengo ndi mwala.’
Koma zimene mukuganizazo sizidzachitika. 33 Ndithu pali Ine wamoyo,
akutero Ambuye Yehova, ndi dzanja langa lamphamvu, nditasamula
mkono wanga mokwiya kwambiri, Ine ndidzakhala wokulamulani.
34 Ndidzakuchotsani pakati pa anthu a mitundu ina ndikukusonkhanitsani
kuchokera ku mayiko kumene munamwazikirako, ndi dzanja langa lam-
phamvu ndi lotambasuka ndili wokwiya kwambiri. 35 Ndidzakulowetsani
m’chipululu cha anthu a mitundu ina ndipo kumeneko, moonana maso
ndi maso, ndidzakuzengani mlandu. 36 Monga ndinawalangira makolo
anu m’chipululu cha dziko la Igupto, motero ndidzakulangani, akutero
Ambuye Yehova. 37 Ndidzakuwerengani ndi ndodo ya m’busa, kukulowet-
sani m’chimango cha pangano langa. 38 Ndidzakuchotserani anthu amene
anandigalukira ndi kundiwukira. Ngakhale ndidzawatulutsa m’dziko
limene akukhalamo, koma sadzalowamo m’dziko la Israeli. Pamenepo
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.
39 “ ‘Koma inu Aisraeli, zimene ndikunena Ine Ambuye Yehova ndi izi:
Pitani katumikireni mafano anu onse, aliyense wa inu! Koma m’tsogolo
mwake mudzandimvera ndithu ndipo simudzayipitsa dzina langa lopat-
ulika popereka mphatso zanu kwa mafano. 40 Pakuti pa phiri langa
lopatulika, phiri lalitali la ku Israeli, akutero Ambuye Yehova, Aisraeli
onse adzanditumikira, ndipo kumeneko Ine ndidzawalandira. Kumeneko
ndidzayembekeza zopereka zanu ndi mphatso zanu zopambana, pamodzi
ndi nsembe zanu zonse zopatulika. 41 Ndidzakulandirani ngati nsembe
ya fungo lokoma ndikadzakutulutsani pakati pa anthu a mitundu ina ndi

kukusokhanitsani kuchokera ku mayiko kumene munabalalitsidwirako.
Motero ndidzadzionetsa pakati panu kuti ndine woyera ndipo mitundu ya
anthu idzaona. 42 Tsono mudzadziwa kuti ndine Yehova ndikadzabwera
nanu ku dziko la Israeli, dziko limene ndinalumbira kuti ndidzapereka
kwa makolo anu. 43 Kumeneko mudzakumbukira makhalidwe anu ndi ma-
chitidwe anu onse amene munadziyipitsa nawo, ndipo mudzanyansidwa
nokha chifukwa cha zoyipa zimene munachita. 44 Inu mudzadziwa kuti
Ine ndine Yehova, ndikadzakuchitirani zabwino chifukwa cha dzina langa
koma osati molingana ndi njira zanu zoyipa ndi machitidwe anu okhota,
inu Aisraeli, akutero Ambuye Yehova.' "

*Uneneri Wotsutsa Kummwera*

45 Yehova anandiyankhula nati: 46 "Iwe mwana wa munthu, tembenuka
uyang'ane kummwera; ndipo lalika mawu odzudzula anthu akummwera
ndipo unenere zodzudzula dziko la nkhalango ya kummwera. 47 Iwuze
nkhalango yakummwera kuti, 'Imvani mawu a Yehova! Ambuye
Yehova akuti: Ndikuyatsa moto ndipo motowo udzapsereza mitengo
yako yonse yayiwisi ndi yowuma yomwe. Malawi ake sadzazimitsika
ndipo aliyense kuchokera kummwera mpaka kumpoto adzapsa nawo.
48 Aliyense adzadziwa kuti Ine Yehova ndi amene ndayatsa motowo, ndipo
sudzazimitsidwa.' "

49 Ndipo ine ndinati, "Aa, Ambuye Yehova! Anthu akungondinena kuti,
'Kodi suja amangonena nthano chabe ameneyu!' "

# 21

*Babuloni, Lupanga la Mulungu*

1 Yehova anandiyankhula nati: 2 "Iwe mwana wa munthu, tembenuka
uyang'ane ku Yerusalemu ndipo ulalike mawu odzudzula malo ake
opatulika. Unenere zodzudzula anthu a ku Yerusalemu. 3 Uwawuze kuti,
Ambuye Yehova akuti, 'Taona, Ine ndidzalimbana nawe. Ndidzasolola
lupanga langa m'chimake ndi kuwononga anthu olungama ndi ochimwa
omwe. 4 Motero ndidzapha aliyense kuchokera kummawa mpaka
kumpoto. 5 Pamenepo anthu onse adzadziwa kuti Ine Yehova ndi amene
ndasolola lupanga langa m'chimake; sindidzalilowetsanso m'chimakemo.'

6 "Tsono iwe mwana wa munthu, buwula. Buwula pamaso pawo ndi
mtima wosweka ndi wachisoni chachikulu. 7 Ndipo akadzakufunsa kuti,
'N'chifukwa chiyani ukubuwula?' Iwe udzayankhe kuti, 'Ndikubuwula
chifukwa cha nkhani imene ndamva. Zikadzachitika zimenezi, mitima
yonse idzangoti fumu, manja onse adzangolefuka, mpweya wawo udza-
wathera, ndipo mawondo onse adzangoti zii.' Izi zikubwera! Ndipo
zidzachitika ndithu, akutero Ambuye Yehova."

8 Yehova anandiyankhulanso kuti, 9 "Iwe mwana wa munthu, unenere
ndipo unene kuti, Ambuye Yehova akuti,

"Izi ndi zimene Yehova akunena:
Lupanga, lupanga, lanoledwa ndipo lapukutidwa.
10 Lanoledwa kuti likaphe,
lapukutidwa kuti ling'anime ngati mphenzi!

" 'Kodi tingakondwere bwanji? Wanyoza ndodo, mwana wanga ndi
chilichonse cha mtengo.

11 " 'Lupanga laperekedwa kuti lipukutidwe,
ndi kuti linyamulidwe,
lanoledwa ndi kupukutidwa,

kuti liperekedwe m'manja mwa munthu amene amapha.
12 Fuwula ndi kulira, iwe mwana wa munthu,
pakuti zimenezi zidzagwera anthu anga;
zidzagweranso akalonga onse a Israeli.
Adzaphedwa ndi lupanga
pamodzi ndi anthu anga.
Chifukwa chake udzigugude pa chifuwa ndi chisoni.
13 " 'Ambuye Wamphamvuzonse akuti: Ndikuwayesa anthu anga, ndipo
ngati satembenuka mtima, ndiye kuti zimenezi sizidzalephera kuwagw-
era.'
14 "Tsono mwana wa munthu, nenera
ndipo uwombe m'manja.
Lupanga likanthe kawiri
ngakhale katatu.
Limenelo ndilo lupanga lophera anthu.
Inde ndilodi lupanga lophera anthu koopsa
limene likuwazungulira.
15 Ndawayikira pa zipata zawo zonse
lupanga laphuliphuli
kuti ataye mtima
ndiponso kuti anthu ambiri agwe.
Aa! Lapangidwa lupanga kuti lizing'anima ngati mphenzi
ndi kuti azilisolola kuphera anthu.
16 Iwe lupanga, ipha anthu kumanja,
kenaka kumanzere,
kulikonse kumene msonga yako yaloza.
17 Inenso ndidzawomba m'manja mwanga,
ndipo ndidzaziziritsa ukali wanga
Ine Yehova ndayankhula."
18 Yehova anandiyankhulanso kuti, 19 "Iwe mwana wa munthu, ulembe
zizindikiro za misewu iwiri imene lupanga la mfumu ya ku Babuloni
lingathe kudzeramo. Misewu yonse ikhale yochokera m'dziko limodzi. Ika
chikwangwani pa mphambano yopita mu mzinda. 20 Ulembe chizindikiro
pa msewu umene lupanga lidzadzere popita ku Raba wa ku Amoni,
ndiponso ku Yuda ndi ku Yerusalemu, mzinda wotetezedwa. 21 Pakuti
mfumu ya ku Babuloni yayima pa msewu, pa mphambano ya misewu
iwiriyo. Ikuwombeza ndi mivi yake kuti idziwe njira yoyenera kudzeramo.
Ikupempha nzeru kwa milungu yake ndipo ikuyang'ana chiwindi cha
nyama yoperekedwa ku nsembe. 22 M'dzanja lake lamanja muli muvi
waula wolembedwa Yerusalemu. Kumeneko mfumuyo idzayika zida
zogumulira, idzalamula kupha anthu ndiponso kufuwula mfuwu wa
nkhondo. Mfumuyo idzapanga zida zogumulira makoma, kuwunda
mitumbira ya nkhondo ndi kumanga nsanja za nkhondo. 23 Koma
kwa anthu a ku Yerusalemu zidzaoneka ngati zowombeza zabodza
chifukwa cha malumbiro amene anachita kwa mfumuyo. Koma mfumuyo
idzawakumbutsa za zolakwa zawo kuti atengedwe ku ukapolo.
24 "N'chifukwa chake Ambuye Yehova akuti, 'Popeza mwandikumbutsa
zolakwa, moti kundiwukira kwanu kwaonekera poyera ndi kuti mu
zochita zanu zonse mukuonetsa machimo anu, n'chifukwa chake mudza-
gwidwa ndi kutengedwa ukapolo.
25 " 'Tsono iwe kalonga wonyozedwa ndi woyipa wa Israeli, amene tsiku
lako lafika, amene nthawi yako yolangidwa yafika penipeni, 26 Ambuye

Yehova akuti: Vula nduwira, chotsa chipewa chaufumu. Zinthu sizidza-
khala monga zinalili: anthu wamba adzakwezedwa ndipo okwezedwa
adzatsitsidwa. 27 Chipasupasu! Chipasupasu! Ine ndidzawupasula
mzindawo! Ndipo sadzawumanganso mpaka atafika amene ali woyenera
kuwulandira; Ine ndidzawupereka kwa iyeyo.’

28 “Ndipo iwe mwana wa munthu, nenera kuti, ponena za Aamoni ndi
zonyoza zawo, Ambuye Yehova akuti,

“ ‘Lupanga, lupanga,
alisolola kuti liphe anthu,
alipukuta kuti liwononge
ndi kuti ling’anime ngati mphenzi.
29 Zimene akuti akuona m’masomphenya zokhudza inu ndi zabodza.
Mawula awo okhudza inu ndi abodzanso.
Mudzakhala pamodzi ndi anthu oyipa
amene tsiku lawo lafika,
ndiye kuti nthawi
ya kulangidwa kwawo komaliza.

30 “ ‘Bwezerani lupanga m’chimake.
Ku malo kumene inu munabadwira,
m’dziko la makolo anu,
ndidzakuweruzani.
31 Ndidzakhuthula ukali wanga pa inu,
ndipo mkwiyo wanga udzakuyakirani.
Ndidzakuperekani m’manja mwa anthu ankhanza;
anthu odziwa bwino kuwononga zinthu.
32 Mudzakhala ngati nkhuni pa moto.
Ena adzakhetsa magazi anu m’dziko lanu lomwe.
Simudzakumbukiridwanso
pakuti Ine Yehova ndayankhula.’ ”

# 22

*Machimo a Yerusalemu*

1 Yehova anandiyankhula nati: 2 “Iwe mwana wa munthu, kodi
udzaweruza mzinda uwo wa anthu akupha anzawo? Tsono uwudzudzule
chifukwa cha machitidwe ake onse onyansa 3 ndipo unene kuti, ‘Ambuye
akuti: Iwe mzinda umene wadzigwetsa wekha m’tsoka pa kukhetsa
magazi pakati pako ndi kudziyipitsa popanga mafano, 4 wapezekatu
wolakwa chifukwa cha magazi amene wakhetsa, ndipo wadziyipitsa
chifukwa cha mafano amene wapanga. Choncho wachepetsa masiku ako,
ndipo zaka zako zafika kumapeto. N’chifukwa chake ndalola kuti anthu
a mitundu ina akunyoze ndiponso kuti anthu a mayiko onse akuseke.
5 Mayiko amene ali pafupi ndi mayiko omwe ali kutali adzakunyoza, iwe
mzinda wa mbiri yoyipa, wodzaza ndi chiwawa.

6 “ ‘Taona momwe aliyense wa atsogoleri a Israeli amagwiritsira
mphamvu zake kupha anthu. 7 Mu mzindamo anthu amanyoza abambo
ndi amayi awo. Iwo amapondereza alendo ndi kuzunza ana amasiye ndi
akazi amasiye. 8 Wanyoza zinthu zanga zopatulika ndi kuyipitsa Masabata
anga. 9 Mwa iwe muli anthu onenera anzawo zabodza kuti aphedwe.
Mwa iwe mulinso amene amadyera zansembe pa mapiri a chipembedzo.
Enanso amachita zonyansa. 10 Mwa iwe muli ena ogonana ndi akazi a

abambo awo, muli enanso amene amavuta akazi pamene ali woyipitsidwa
ndi msambo. [11] Ena amachita chigololo ndi akazi a anzawo, ndipo ena,
mopanda manyazi, amayipitsa mkazi wa mwana wawo. Palinso ena
amene amayipitsa alongo awo, ana aakazi a abambo awo. [12] Mwa iwe
muli anthu amene amalandira ziphuphu kuti aphe anzawo; ena amachita
katapira ndi kupeza phindu loposera muyeso; enanso amapeza phindu
mwachinyengo poopseza anzawo. Ndipo mwandiyiwala Ine, akutero
Ambuye Yehova.

[13] " 'Koma Ine ndachita kuwomba m'manja kuti phuu n'kudabwa
chifukwa cha phindu lachinyengo limene mwapeza ndiponso chifukwa
cha kuphana kumene kumachitika pakati panu. [14] Kodi mtima wako udza-
khala wolimbabe kapena manja ako adzakhalabe amphamvu ndikadzat-
siriza kukulanga iwe? Ine Yehova ndayankhula, ndipo ndidzazichitadi.
[15] Ndidzakubalalitsani pakati pa anthu a mitundu ina ndi kukumwazi-
rani ku mayiko onse. Umu ndi mmene ndidzachotsere zoyipa zako.
[16] Udzanyozedwa pamaso pa anthu a mitundu ina. Pambuyo pake
udzadziwa kuti Ine ndine Yehova.' "

[17] Yehova anandiyankhula nati: [18] "Iwe mwana wa munthu, Aisraeli
asanduka chinthu cha chabechabe kwa Ine. Onse ali ngati mkuwa, chitini,
chitsulo ndi mtovu zotsala m'ng'anjo atayeretsa siliva. [19] N'chifukwa
chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: 'Pakuti nonse mwasanduka chinthu
cha chabechabe, Ine ndidzakusonkhanitsani mu Yerusalemu. [20] Monga
momwe anthu amasonkhanitsira siliva, mkuwa, chitsulo, mtovu ndi
chitini m'ng'anjo ndi kusonkhetsa moto kuti azisungunule, motero Inenso
ndidzakusonkhanitsani ndili wokwiya ndi waukali, ndipo ndidzakuyikani
m'kati mwa mzinda, ndikukusungunurani. [21] Ndidzakusonkhanitsani
mu mzindamo ndi kukoleza moto wa mkwiyo wanga, ndipo inu
mudzasungunuka mu mzindamo. [22] Monga siliva amasungunulidwa
m'ng'anjo, kotero inunso mudzasungunuka m'kati mwa mzinda ndipo Inu
mudzadziwa kuti Ine Yehova ndakukwiyirani.' "

[23] Yehova anandiyankhulanso nati, [24] "Iwe mwana wa munthu,
uza dziko la Israeli kuti, 'Iwe ndiwe dziko losayeretsedwa, ndiponso
losavumbidwa ndi mvula chifukwa cha mkwiyo wanga.' [25] Atsogoleri ake
mu mzindamo ali ngati mkango wobangula pogwira nyama. Apha anthu,
alanda chuma ndi zinthu za mtengowapatali, ndiponso asandutsa amayi
ambiri kukhala amasiye. [26] Ansembe ake amaphwanya lamulo langa ndi
kuyipitsa zinthu zanga zopatulika. Sasiyanitsa pakati pa zinthu zopatulika
ndi zinthu wamba. Saphunzitsa anthu kusiyana kwa zinthu zoyenera pa
chipembedzo ndi zinthu zosayenera. Sasamalira za kusunga masabata
anga. Motero Ine ndimanyozedwa pakati pawo. [27] Atsogoleri ake ali
ngati mimbulu yokhadzula nyama; amakhetsa magazi ndi kupha anthu
kuti apeze phindu loyipa. [28] Aneneri ake amabisa zonsezi monga muja
amachitira anthu popaka njereza. Amazimphimba ndi zabodza zimene
aona m'masomphenya awo ndi zonama za m'mawula awo. Iwo amati,
'Ambuye Yehova akuti,' pamene Ine Yehova sindinayankhule. [29] Anthu
a m'dzikomo amasautsa anzawo ndi kulanda anthu osowa. Amazunza
anthu osauka ndi amphawi. Amavutitsa alendo posawachitira zinthu
mwachilungamo.

[30] "Ndinafunafuna munthu pakati pawo woti amange linga, woti
ayimirire dziko pamaso panga kundipepesa kuti ndisaliwononge, koma

sindinamupeze. [31] N'chifukwa chake ndawakwiyira kwambiri. Ndawa-
wonongeratu ndi mkwiyo wanga woyaka ngati moto. Ndawalanga
molingana ndi zimene anachita. Akutero Ambuye Yehova."

# 23

*Za Yerusalemu ndi Samariya*

[1] Yehova anandiyankhula nati: [2] "Iwe mwana wa munthu, panali
atsikana awiri ana a mayi mmodzi. [3] Iwo ankachita za chiwerewere
ku Igupto. Za chiwerewerezo anayamba ali achichepere. Kumeneko
anthu ankangowasisita pa chifuwa ndi kuwagwiragwira mawere awo aja.
[4] Wamkulu dzina lake anali Ohola, ndipo mng'ono wakeyo anali Oholiba.
Ine ndinawakwatira ndipo anabereka ana aamuna ndi ana aakazi. Ohola
ndiye Samariya, ndipo Yerusalemu ndiye Oholiba.

[5] "Ohola anachita zachiwerewere ngakhale anali mkazi wanga; ndipo
iye anakangamira abwenzi ake a ku Asiriya. [6] Amenewo anali asi-
likali ovala zibakuwa zamlangali, abwanamkubwa ndiponso atsogoleri a
nkhondo. Onsewo anali anyamata osiririka ndipo ankakwera pa akavalo.
[7] Ohola anachita zachiwerewere ndi onsewa, anthu otchuka a ku Asiriya.
Iye anadziyipitsa ndi mafano a munthu aliyense amene anagona naye.
[8] Iye sanaleke za chiwerewere zimene anaziphunzira ku Igupto. Paja
akanali mtsikana anyamata ankagona naye. Iwo ankamusisita mawere
akanali anthete nachita naye zachiwerewere.

[9] "N'chifukwa chake Ine ndinamupereka kwa achikondi ake, Asiriya,
amene iye ankawalakalaka. [10] Iwowa anamuvula, namulanda ana ake
aamuna ndi aakazi ndipo anamupha ndi lupanga. Ndipo atalangidwa
choncho, iye anasanduka chinthu chonyozeka pakati pa akazi.

[11] "Mphwake Oholiba anaona zimenezi natengerako. Koma iye anachita
zachiwerewere kuposa mkulu wake. [12] Iyenso anakangamira Asiriya,
abwanamkubwa, olamulira asilikali, ankhondo ovala zovala zonse za
nkhondo ndi okwera pa akavalo. Onsewa anali anyamata osiririka.
[13] Ndinaona kuti iyenso anadziyipitsa; ndipo onse awiriwo anatsata njira
imodzi.

[14] "Koma Oholiba uja anachita chigololo kopitirira mkulu wake. Iye
anaona zithunzi za amuna pa khoma, zithunzi za Ababuloni zolem-
bedwa ndi inki yofiira, [15] atamanga malamba m'chiwuno mwawo ndi
kuvala nduwira pa mitu yawo. Onse amaoneka ngati atsogoleri a
magaleta a Ababuloni, mbadwa za ku Kaldeya. [16] Oholiba atangowaona,
anawalakalaka ndipo anatuma amithenga ku Kaldeya kukawayitana.
[17] Ndipo Ababuloni anabwera n'kudzagona naye. Choncho mwa chilako-
lako chawo anamuyipitsa. Koma atamuyipitsa choncho, iye ananyan-
sidwa nawo. [18] Iye atachita chiwerewere chake poyera ndi kuonetsa
umaliseche wake, Ine ndinamuchokera monyansidwa monga mmene
ndinachitira ndi m'bale wake. [19] Koma anachitabe zachiwerewere
osalekeza. Ankakumbukira masiku a ubwana wake pamene ankachita za
chiwerewere m'dziko la Igupto. [20] Kumeneko iye ankalakalaka zibwenzi
zake, amene ziwalo zawo zinali ngati za abulu ndipo kutentha kwawo
kunali ngati kwa akavalo. [21] Motero, iwe Oholiba unafuna kuchitanso
zadama monga unkachitira ku Igupto pamene unali mtsikana. Nthawi
imene ija ankakusisita pa chifuwa ndi kugwiragwira mawere ako osagwa
aja.

22 “Tsono iwe Oholiba, Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ndidzakudzutsira
zibwenzi zako zimene unkanyansidwa nazo zija kuti zilimbane nawe.
Ndidzaziyitana kuti zibwere kuchokera mbali zonse. 23 Ndidzayitana
anthu a ku Babuloni ndi Akaldeya onse, anthu a ku Pekodi, Sowa
ndi Kowa pamodzi ndi Asiriya onse. Onsewa ndi amuna osiririka,
abwanamkubwa, atsogoleri a ankhondo, oyenda pa magaleta, anthu a
maudindo akuluakulu. Onsewa ndi okwera akavalo. 24 Iwo adzabwera
kudzalimbana nawe ndi zida za nkhondo, magaleta ndi ngolo, pamodzi
ndi anthu ambiri. Adzakuzinga mbali zonse atavala zishango zankhondo
ndi zipewa zankhondo. Ndidzakupereka kwa iwo kuti akulange ndipo
adzakulanga monga momwe adzafunire. 25 Ndidzaonetsa mkwiyo wanga
pa iwe ndipo iwo adzakulanga iwe mwankhanza. Adzadula mphuno
zanu ndi makutu anu, ndipo amene adzatsalira mwa iwe adzaphedwa
ndi lupanga. Iwo adzakulanda ana ako aamuna ndi aakazi ndipo amene
adzatsalira adzaphedwa ndi moto. 26 Adzakuvulaninso zovala zanu
ndikukulandani zodzikongoletsera zanu zamtengowapatali. 27 Motero
ndidzathetsa zonyansa zako ndi zachigololo zomwe unaziyamba ku
Igupto. Choncho sudzalakalaka za ku Igupto kapena kuzikumbukiranso.

28 “Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ndikukupereka m’manja mwa
amene amadana nawe, kwa iwo amene unawafulatira moyipidwa nawo.
29 Adzachita nawe mwachidani. Adzakulanda zonse zimene unagwirira
ntchito. Adzakusiya wamaliseche ndiponso wausiwa. Kuyipa kwa
makhalidwe ako achiwerewere kudzakhala pammbalambanda. Zonyansa
zako ndi chiwerewere chako, 30 zabweretsa izi pa iwe chifukwa una-
chita zonyansa ndi anthu a mitundu ndi kudziyipitsa ndi mafano awo.
31 Unatsata zochita za mkulu wako; choncho Ine ndidzayika chikho cha
chilango chake m’dzanja lako.

32 “Ine Ambuye Yehova ndikuti:
“Udzamwera chikho cha mkulu wako,
chikho chachikulu ndi chakuya;
anthu adzakuseka ndi kukunyoza,
pakuti chikhocho ndi chodzaza kwambiri.
33 Udzaledzera ndipo mtima wako udzadzaza ndi chisoni.
Chimenechi ndi chikho chachiwonongeko ndi chipasupasu,
chikho cha mkulu wako Samariya.
34 Udzamwa chikhocho mpaka kugugudiza.
Tsono udzaphwanyaphwanya chikhocho
ndipo udzang’amba mawere ako ndi zigoba zake.
Ine ndayankhula, akutero Ambuye Yehova.

35 “Chifukwa chake, Ine Ambuye Yehova ndikuti: Popeza wandiyiwala
Ine ndi kundifulatira, chomwecho uyenera kulangidwa chifukwa cha
zonyansa zako ndi chiwerewere chako.”

36 Yehova anandifunsa kuti, “Iwe mwana wa munthu, kodi udza-
weruza Ohola ndi Oholiba? Tsono uwayimbe mlandu chifukwa cha
machitidwe awo onyansa. 37 Iwo achita chigololo ndipo anapha anthu.
Anachita chigololo popembedza mafano awo. Ngakhale ana amene
anandiberekera Ine anawapereka kwa mafanowo ngati chakudya chawo.
38 Anachitanso izi: Iwo anayipitsa malo anga opatulika ndi kudetsa
masabata anga. 39 Atapereka ana awo kwa mafano, tsiku lomwelo
anakalowanso m’Nyumba yanga yopatulika ndi kuyipitsamo. Izi ndi
zimene anachita m’Nyumba mwanga.

40 “Iwo anatuma amithenga kukayitana amuna a ku mayiko aku-
tali. Anthuwo atabwera, abale awiri aja anasambasamba, kudzola
utoto wodzikometsera kumaso, kenaka ndi kuvala zovala zamakaka.
41 Anakhala pa bedi lokongola ndipo patsogolo pawo panali tebulo pamene
munayikapo lubani ndi mafuta. Zonse zowapatsa Ine.

42 “Mfuwu wa chigulu cha anthu unamveka. Anthu oledzera ochokera
ku chipululu anabwera pamodzi ndi anthu wamba ndipo anaveka akaziwo
zibangiri kumanja ndi zipewa zaufumu zokongola ku mutu. 43 Ndipo ine
ndinati za mkazi wotheratu ndi chigololoyo, ‘Tsono asiyeni kuti achite
naye monga wachiwerewere, pakuti ichi ndi chimene iye ali basi.’ 44 Tsono
anapita kwa iwo monga mmene anthu amapitira kwa mkazi wadama.
Momwemo anapita kwa Ohola ndi kwa Oholiba kukachita nawo zadama.
45 Koma anthu olungama adzawazenga anthuwa mlandu wa chigololo ndi
wa kupha anthu. Ndi iwodi anthu achigololo ndiponso m’manja mwawo
muli magazi.

46 “Ambuye Yehova akuti: Itanitsani chigulu cha anthu kuti chidza-
walange ndi kulanda chuma chawo. 47 Anthuwo adzawaponye miyala
akazi awiriwo ndi kuwatema ndi malupanga awo. Ana awo aamuna ndi
aakazi adzawaphe ndi kutentha nyumba zawo.

48 “Motero Ine ndidzathetsa zachigololo m’dzikomo, ndipo akazi onse
adzatengapo phunziro kuti asadzachite zachigololo monga za iwowo.
49 Ndidzawalanga chifukwa cha ntchito zawo za dama ndipo adzazunzika
chifukwa cha tchimo lawo lopembedza mafano. Choncho adzadziwa kuti
Ine ndine Ambuye Yehova.”

# 24

### *M’phika Wophikira*

1 Pa tsiku lakhumi la mwezi wakhumi chaka chachisanu ndi chinayi,
Yehova anandiyankhula kuti: 2 “Iwe mwana wa munthu lemba dzina la
tsiku lalero, lero lomwe lino, chifukwa mfumu ya Babuloni yazungulira
Yerusalemu lero lino. 3 Uwaphere mwambi anthu owukirawa ndi
kuwawuza kuti: ‘Ambuye Yehova akuti,
“ ‘Ikani m’phika pa moto,
ndipo mu m’phikamo muthiremo madzi.
4 Mu m’phikamo muyikemo nthuli za nyama,
nthuli zonse zabwino kwambiri za mwendo wathako ndi mwendo wamwamba.
Mudzadzemo mafupa abwino kwambiri.
5 Pa gulu la nkhosa musankhepo nkhosa yabwino kwambiri.
Muyike nkhuni pansi pa m’phikawo.
Madzi awire.
Kenaka muphike nyamayo pamodzi ndi mafupa omwe.’

6 “ ‘N’chifukwa chake, Ambuye Yehova akuti,
“ ‘Tsoka kwa mzinda wokhetsa magazi,
tsoka kwa m’phika wadzimbiri;
dzimbiri lake losachoka!
Mutulutsemo nthuli imodzimodzi
osasankhulapo.

7 “ ‘Paja magazi amene anakhetsa akanali pakati pake mu mzindamo.

Iye awakhuthulira pa thanthwe losalala.
Sanawakhutulire pa dothi
kuopa kuti fumbi lingawafotsere.
8 Ndinasiya magaziwo pa mwala wosalala
kuti asafotseredwe ndi fumbi
chifukwa ndinafuna kuonetsa mkwiyo wanga ndi kulipsira.

9 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti:
" 'Tsoka kwa mzinda wokhetsa magazi!
Inenso, ndidzawunjika mulu waukulu wa nkhuni.
10 Choncho wonjeza nkhuni
ndipo muyatse moto.
Phikani nyamayo bwinobwino,
muthiremo zokometsera,
mutsanule msuzi, ndipo mupsereze mafupawo.
11 Tsono muyike pa makala m'phika wopanda kanthuwo
mpaka utenthe kuchita kuti psuu
kuti zonyansa zake zisungunuke
ndi kuti dzimbiri lake lichoke.
12 Koma m'phikawo walephereka kuyeretsedwa.
Dzimbiri lake linalowerera silingatheke kuchoka
ngakhale ndi moto womwe.
13 " 'Tsono dzimbiri limeneli ndi zilakolako za dama lako. Pakuti ine
ndinayesa kukutsuka koma iwe sunayere, ndipo sudzayeranso mpaka
ukali wanga utakwaniratu pa iwe.

14 " 'Ine Yehova ndayankhula. Zimenezi zikubwera ndipo ndidzazichi-
tadi. Sindidzabwerera m'mbuyo. Sindidzakulekerera kapena kukuchitira
chifundo. Ndidzakulanga molingana ndi makhalidwe ndi machitidwe ako,
akutero Ambuye Yehova.' "

### *Imfa ya Mkazi wa Ezekieli*

15 Yehova anandiyankhula kuti: 16 "Iwe mwana wa munthu, Ine
ndikulanda mwadzidzidzi mkazi amene amakukomera m'maso kwambiri.
Koma usadandaule, usalire kapena kukhetsa misozi. 17 Ubuwule koma
mwakachetechete. Usamulire wakufayo. Uvale nduwira yako ndithu,
nsapato zakonso usavule. Usaphimbe nkhope kapena kudya chakudya
cha anamfedwa."
18 Choncho ndinayankhula ndi anthu mmawa, ndipo madzulo mkazi
wanga anamwalira. Mmawa mwake ndinachita monga momwe anandil-
amulira.
19 Ndipo anthu anandifunsa kuti, "Kodi sutifotokozera tanthauzo la
zimene ukuchitazi?"
20 Ndinawayankha kuti, "Yehova anandipatsa uthenga wakuti, 21 'Awuze
Aisraeli kuti: Ine Ambuye Yehova ndikuti: ndidzayipitsa Nyumba yanga
yopatulika, nyumba imene mwakhala mukuyinyadira. Mumakondwa
kwambiri poyiona, ndipo mumayikonda ndi mtima onse. Ana aamuna ndi
aakazi amene munawasiya m'mbuyo adzaphedwa ndi lupanga. 22 Ndipo
mudzachita monga ndachitira inemu. Inu simudzaphimba nkhope zanu
kapena kudya chakudya cha anamfedwa. 23 Mudzavala nduwira zanu
kumutu ndi nsapato zanu ku mapazi anu. Simudzabuma maliro kapena
kukhetsa misozi koma mudzavutika kwambiri chifukwa cha machimo anu
ndipo mudzabuwula pakati panu. 24 Ine Ezekieli ndidzakhala chitsanzo

chanu. Mudzachita monga momwe ndachitira. Izi zikadzachitika, akutero Yehova, ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Ambuye Wamphamvuzonse.'
25 "Ndipo Yehova anandiyankhula nati: Iwe mwana wa munthu, tsiku lina ndidzawachotsera anthuwa linga lawo limene ankakondwerera kukongola kwake, limene linkawakomera m'maso mwawo, limenenso anayikapo mtima wawo kwambiri. Ndidzawachotsera ana awo aamuna ndi aakazi.
26 Pa tsiku limenelo wothawa nkhondo adzabwera kudza-kuwuzani zimenezo.
27 Pa tsiku limenelo pakamwa pako padzatsekuka. Udzatha kuyankhula naye ndipo sudzakhalanso chete. Motero udzakhala chizindikiro kwa iwo, ndipo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

# 25

*Za Chilango cha Aamoni*

1 Yehova anandiyankhula kuti:
2 "Iwe mwana wa munthu, tembenukira anthu a ku Amoni ndipo unenere mowadzudzula.
3 Awawuze kuti, 'Inu anthu a ku Amoni, imvani zimene Ambuye Yehova akunena. Iye akuti: Inu munanena mawu onyoza pamene Nyumba yanga yopatulika inkayipitsidwa. Munanyozanso dziko la Israeli pamene linaguga ndiponso anthu a ku Yuda pamene anatengedwa ukapolo.
4 N'chifukwa chake Ine ndidzakuperekani m'manja mwa anthu akummawa ngati cholowa chawo. Iwo adzamanga misasa yawo ndi kukhoma matenti awo pakati panu. Adzadya zipatso zanu ndi kumwa mkaka wanu.
5 Ndidzasandutsa Raba kuti akhale busa la ngamira ndi mizinda ya Aamoni kuti ikhale makola a nkhosa. Pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.
6 Zimene ndikunena Ine Ambuye Yehova ndi izi: Inu munawomba m'manja ndi kumalumphalumpha. Munkakondwa mu mtima mwanu pamene munkanyoza dziko la Israeli.
7 N'chifukwa chake ndidzatambasula dzanja langa kuti ndikulangeni, ndipo ndidzakuperekani kuti mukhale chofunkha cha anthu a mitundu ina. Ndidzakuchotsani pakati pa anthu a mitundu ina ndi kukufafanizani m'mayiko onse. Ndidzakuwonongani, ndipo inu mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova!' "

*Za Chilango cha Mowabu*

8 "Ambuye Yehova akuti, 'Anthu a ku Mowabu ndi a ku Seiri ananena kuti anthu a ku Yuda ali ngati mayiko ena onse.'
9 N'chifukwa chake ndidzagumula mbali ina ya Mowabu, kuyambira ku mizinda yake ya kumalire; mizinda yokongola ya Beti-Yesimoti, Baala-Meoni ndi Kiri-ataimu.
10 Ndidzapereka Amowabu pamodzi ndi Aamoni m'manja mwa anthu akummawa kotero kuti Aamoni adzayiwalikiratu pakati pa anthu a mitundu ina.
11 Ndidzawalangadi Amowabuwo. Pamenepo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

*Za Chilango cha Edomu*

12 "Ambuye Yehova akuti, 'Pakuti Edomu analipsira Ayuda, ndiye kuti analakwa kwambiri pochita zimenezi.
13 N'chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ndidzatambasula dzanja langa kulanga Edomu ndi kupha anthu ake ndiponso nyama zawo. Ndidzawonongeratu Edomu ndipo adzaphedwa ndi lupanga kuchokera ku Temani mpaka ku Dedani.
14 Ndidzalanga Edomu ndi dzanja la anthu anga Aisraeli. Adzalanga anthu a ku Edomu molingana ndi mkwiyo ndi ukali wanga. Choncho adzaona kulipsira kwanga akutero Ambuye Yehova.' "

*Za Chilango cha Filisitiya*

15 “Ambuye Yehova akuti, ‘Afilisti analanga anthu anga mwankhanza
ndi kuwalipsira. 16 N’chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti:
Ndidzatambasula dzanja langa kukantha Afilistiwo. Ndidzafafaniza
Akereti ndi kuwononga iwo amene amakhala m’mbali mwa nyanja.
17 Ndidzawabwezera chilango choopsa ndipo ndidzawalanga mu mkwiyo
wanga. Ndikadzawalipsira ndipo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.’ ”

# 26

*Za Chilango cha Turo*

1 Pa chaka cha khumi ndi chimodzi, tsiku loyamba la mwezi, Yehova
anandiyankhula kuti: 2 “Iwe mwana wa munthu, anthu a ku Turo ananyo-
godola Yerusalemu kuti ‘Hii! Uja amene anali chipata choloweramo anthu
a mitundu ina wawonongeka. Zitseko zake zatsekukira ife. Tidzalemera
popeza wasanduka bwinja.’ 3 N’chifukwa chake, Ine Ambuye Yehova
ndikuti: Ndidzakulangani, inu anthu a ku Turo. Ndidzakuyitanirani anthu
a mitundu ina kuti adzakulangeni monga momwe mafunde amawombera
pa Nyanja. 4 Anthuwo adzawononga makoma a Turo ndi kugwetsa nsanja
zake. Ndidzapala dothi lake ndipo ndidzamusandutsa thanthwe losalala.
5 Udzakhala poyanikapo makoka pakati pa nyanja. Ine Ambuye Yehova
ndayankhula zimenezo. Udzasanduka chofunkha cha anthu a mitundu
ina. 6 Anthu okhala ku mtunda adzasakazidwa ndi lupanga. Pamenepo
adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

7 “Ine Ambuye Yehova ndikuti: Iwe Turo, ndidzakubweretsera
Nebukadinezara, mfumu ya ku Babuloni mfumu ya mafumu, kuchokera
kumpoto pamodzi ndi akavalo ndiponso magaleta, anthu okwera pa
akavalo ndi gulu lalikulu la ankhondo. 8 Anthu okhala ku mtunda adza-
wapha ndi lupanga. Adzapanga mitumbira yankhondo ndi kukukwezera
zishango kuti alimbane nawe. 9 Adzagwetsa makoma ako ndi zida zogu-
mulira khoma ndi kugwetsa nsanja zako ndi nkhwangwa zake. 10 Akavalo
ake adzakhala ochuluka kwambiri kotero kuti adzakukwirira ndi fumbi
lawo. Makoma ako adzagwedezeka ndi mdidi wa akavalo, ngolo ndi
magaleta pamene iye adzalowa pa zipata monga mmene amalowera mu
mzinda umene makoma ake agwetsedwa. 11 Akavalo ake adzapondaponda
m’misewu yako yonse ndi ziboda zawo. Adzapha anthu ako ndi lupanga.
Mizati yako yolimba idzagwetsedwa. 12 Iwo adzafunkha chuma chako
ndipo adzalanda zinthu zako za malonda. Adzagwetsa makoma ako ndi
kuwononga nyumba zako zabwino. Adzaponya miyala yako, matabwa ako
ndi dothi lako m’nyanja. 13 Choncho ndidzathetsa phokoso la nyimbo zanu,
ndipo kulira kwa apangwe ako sikudzamvekanso. 14 Ndidzakusandutsa
thanthwe losalala, ndipo udzakhala malo woyanikapo makoka a nsomba.
Sudzamangidwanso, pakuti Ine Yehova ndayankhula, akutero Ambuye
Yehova.

15 “Ine Ambuye Yehova ndikukuwuza, iwe mzinda wa Turo, kuti zilumba
zidzagwedezeka pakumva za kugwa kwako ndiponso poona anthu op-
weteka akubuwula ndipo anthu akuphedwa pakati pako. 16 Pamenepo
mafumu a m’mbali mwa nyanja adzatsika pa mipando yawo yaufumu.
Adzayika pambali mikanjo yawo ndi kuvala zovala zawo zamakaka.
Adzachita mantha ndipo adzakhala pansi akunjenjemera kosalekeza.
Adzathedwa nzeru poona zimene zakugwera. 17 Pamenepo adzayimba
nyimbo yokudandaula ndipo adzati kwa iwe:
“ ‘N’kuchita kuwonongeka chotere, iwe mzinda wotchuka,

wodzaza ndi anthu a ku nyanja!
Unali wamphamvu pa nyanja,
iwe ndi nzika zako;
unkaopseza anthu onse amene
ankakhala kumeneko.
18 Tsopano mayiko a m'mbali mwa nyanja akunjenjemera
chifukwa cha kugwa kwako;
okhala pa zilumba nawonso agwidwa ndi mantha aakulu
chifukwa cha kugwa kwako.'

19 "Mawu a Ine Ambuye Yehova ndi awa: Ndidzakusandutsa bwinja,
ngati mizinda imene anthu sangathe kukhalamo. Ndidzakuphimba
ndi madzi ozama a m'nyanja, madzi amphamvu woti akumize.
20 Ndidzakugwetsa pansi kuti ukhale pamodzi ndi anthu amvulazakale
amene akutsikira ku manda. Ine ndidzakusunga ku dzenjeko ngati ku
bwinja losiyidwa kalekale, pamodzi ndi anthu amene anafa kale motero
sudzabwererako kukhala pakati pa anthu amoyo. 21 Ine ndidzakuthetsa
mochititsa mantha, ndipo sudzakhalaponso. Anthu adzakufunafuna,
koma sudzapezekanso, akutero Ambuye Yehova."

# 27

*Nyimbo Yodandaulira Turo*

1 Yehova anandiyankhula kuti: 2 "Iwe mwana wa munthu, imba nyimbo
yodandaulira Turo. 3 Uza Turo, mzinda wokhala pa dooko la nyanja,
wochita malonda ndi anthu ambiri a m'mbali mwa nyanja kuti: Ambuye
Yehova akuti,
"Iwe Turo, umanena kuti,
'Ndine wokongola kwambiri.'
4 Malire ako anali m'kati mwenimweni mwa nyanja;
amisiri ako anakukongoletsa kwambiri.
5 Anakupanga ndi matabwa
a payini ochokera ku Seniri;
anatenga mikungudza ya ku Lebanoni
kupangira mlongoti wako.
6 Ndi mitengo ya thundu ya ku Basani
anapanga zopalasira zako;
ndi matabwa a mitengo ya payini yochokera ku zilumba za Kitimu.
Pakuti anapanga thandala lako pakati pa matabwawo panali minyanga ya njovu.
7 Nsalu yabafuta yopeta yochokera ku Igupto inali thanga yako,
ndipo inakhala ngati mbendera.
Nsalu zophimba matenti ako zinali za mtundu wamtambo ndi pepo
zochokera ku zilumba za Elisa.
8 Anthu a ku Sidoni ndi Arivadi ndi amene anali opalasa ako.
Anthu aluso ako, iwe Turo, anali mwa iwe ndiwo amene ankakuyendetsa.
9 Akuluakulu ndi eni luso a ku Gebala anali m'kati mwako,
ngati okonza zibowo zako.
Sitima za pa nyanja zonse, ndi oyendetsa ake
ankabwera pamodzi ndi katundu kudzachita nawe malonda.

10 "Anthu a ku Perisiya, a ku Ludi ndi Puti
anali asilikali m'gulu lako la nkhondo.

Iwo ankapachika zishango ndi zipewa zawo zankhondo pa makoma ako,
kubweretsa kwa iwe ulemerero.
11 Anthu a ku Arivadi ndi Heleki
ankalondera mbali zonse za mpanda wako;
anthu a ku Gamadi
anali mu nsanja zako,
Iwo ankapachika zishango zawo pa makoma ako onse.
Amenewo ndiwo anakukongoletsa kwambiri.
12 "Dziko la Tarisisi linachita nawe malonda chifukwa cha kuchuluka
kwa katundu wako wamtundumtundu. Iwo ankapereka siliva, chitsulo,
chitini ndi mtovu mosinthanitsa ndi katundu wako.
13 "Yavani, Tubala ndi Mesaki ankachita nawe malonda; iwo ankapereka
akapolo ndi ziwiya za mtovu mosinthanitsa ndi katundu wako.
14 "Anthu a ku Beti Togarima ankapereka akavalo antchito, akavalo
ankhondo ndi abulu mosinthanitsa ndi katundu wako.
15 "Anthu a ku Dedani ankachita nawe malonda, ndipo anthu ambiri a
m'mbali mwa nyanja anali ogula malonda ako. Ankakupatsa minyanga
ya njovu ndi phingo.
16 "Anthu a ku Aramu ankachita nawe malonda chifukwa cha kuchuluka
kwa zinthu zako. Iwo ankapereka miyala ya emeradi, nsalu zapepo, nsalu
zopetapeta, nsalu zabafuta, korali ndi miyala ya rubi mosinthanitsa ndi
katundu wako.
17 "Yuda ndi Israeli ankachita nawe malonda. Iwo ankapereka tirigu
ochokera ku Miniti ndi zokometsera zakudya, uchi, mafuta ndi mankhwala
mosinthanitsa ndi katundu wako.
18 "Anthu a ku Damasiko, chifukwa cha zinthu zako za malonda
zambiri ndi katundu wako wosiyanasiyana, ankachita nawe malonda a
vinyo wochokera ku Heliboni ndi ubweya wankhosa ochokera ku Zahari.
19 Adani ndi Agriki ochokera ku Uzala ankagula katundu wako. Iwo
ankapereka chitsulo chosalala, kasiya ndi bango lonunkhira mosinthanitsa
ndi katundu wako.
20 "Anthu a ku Dedani ankakugulitsa nsalu zoyika pa zishalo za akavalo.
21 "Arabiya ndi mafumu onse a ku Kedara anali ogula malonda ako. Iwo
ankachita nawe malonda a ana ankhosa onenepa, nkhosa zazimuna ndi
mbuzi.
22 "Anthu amalonda a ku Seba ndi Raama ankachita nawe malonda.
Iwo ankapereka zonunkhira zosiyanasiyana zabwino kwambiri, miyala
yokongola ndi golide mosinthanitsa ndi katundu wako.
23 "Amalonda a ku Harani, Kane, Edeni, Seba, Asuri ndi Kilimadi anka-
chita nawe malonda. 24 Iwowa ankasinthanitsana nawe zovala zokongola,
nsalu zopetapeta, zoyala pansi za mawangamawanga, atazimanga bwino
ndi zingwe zolimba.
25 "Sitima za pa madzi za ku Tarisisi zinali
zonyamula malonda ako.
Motero iwe uli ngati sitima yapamadzi
yodzaza ndi katundu wolemera.
26 Anthu opalasa ako amakupititsa
pa nyanja yozama.
Koma mphepo yakummawa idzakuthyolathyola
pakati pa nyanja.
27 Chuma chako, katundu wako, malonda ako,
okuyendetsa ako, okuwongolera ako ndi opanga sitima za pa madzi,
anthu ako amalonda ndi asilikali ako onse

ndiponso aliyense amene ali m'menemo
adzamira m'nyanja
tsiku limene udzawonongeka.
28 Madera a m'mbali mwa nyanja adzagwedezeka
chifukwa cha kufuwula kwa oyendetsa sitimawo.
29 Onse amene amapalasa sitima zapamadzi,
adzatuluka m'sitima zawo;
oyendetsa ndi onse owongolera sitima zapamadzi
adzayimirira m'mbali mwa nyanja.
30 Iwo akufuwula,
kukulira iwe kwambiri;
akudzithira fumbi kumutu,
ndi kudzigubuduza pa phulusa.
31 Akumeta mpala mitu yawo chifukwa cha iwe
ndipo akuvala ziguduli.
Akukulira iweyo
ndi mitima yowawa kwambiri.
32 Akuyimba nyimbo
yokudandaulira n'kumati:
'Ndani anawonongedwapo ngati Turo
pakati pa nyanja?'
33 Pamene malonda ako ankawoloka nyanja
unakhutitsa mitundu yambiri ya anthu.
Mafumu a dziko lapansi analemera ndi chuma chako
komanso ndi malonda ako.
34 Koma tsopano wathyokera m'nyanja,
pansi penipeni pa nyanja.
Katundu wako ndi onse amene anali nawe
amira pamodzi nawe.
35 Onse amene amakhala m'mbali mwa nyanja
aopsedwa ndi zimene zakuchitikira.
Mafumu awo akuchita mantha
ndipo nkhope zangoti khululu.
36 Anthu amalonda a mitundu ina akukunyogodola.
Watha mochititsa mantha
ndipo sudzakhalaponso mpaka muyaya."

# 28

### *Mawu Odzudzula Mfumu ya Turo*

1 Yehova anandiyankhula nati: 2 "Iwe mwana wa munthu, iwuze mfumu
ya ku Turo mawu a Ine Ambuye Yehova akuti,
" 'Iwe ndi mtima wako wodzikuza
umanena kuti, 'Ine ndine mulungu;
ndimakhala pa mpando wa mulungu
pakati pa nyanja.'
Koma ndiwe munthu chabe osati mulungu,
ngakhale ukuganiza kuti ndiwe wanzeru ngati mulungu.
3 Taona, ndiwedi wanzeru kupambana Danieli.
Ndipo palibe chinsinsi chobisika kwa iwe.
4 Mwa nzeru zako ndi kumvetsa kwako
unadzipezera chuma
ndipo unasonkhanitsa golide ndi siliva

m’nyumba zosungira chuma chako.
5 Ndi nzeru zako zochitira malonda
unachulukitsa chuma chako
ndipo wayamba kunyada
chifukwa cha chuma chakocho.
6 “ ‘Choncho Ine Ambuye Yehova ndikuti,
“ ‘Popeza umadziganizira
kuti ndiwe mulungu,
7 Ine ndidzabwera ndi anthu achilendo, anthu ankhanza,
kuti adzalimbane nawe.
Adzakuthira nkhondo kuti awononge zonse zimene unazipeza ndi nzeru zako,
ndipo adzawononga kunyada kwakoko.
8 Iwo adzakuponyera ku dzenje
ndipo udzafa imfa yoopsa
m’nyanja yozama.
9 Kodi udzanenabe kuti, ‘Ine ndine mulungu,’
pamaso pa iwo amene akukupha?
Iwe udzaoneka kuti ndiwe munthu chabe, osati mulungu,
m’manja mwa iwo amene akukuphawo.
10 Udzafa imfa ya anthu osachita mdulidwe
m’manja mwa anthu achilendo.
Ine ndayankhula zimenezi, akutero Ambuye Yehova.’ ”

11 Yehova anandiyankhula kuti: 12 “Iwe mwana wa munthu, imba
nyimbo yodandaulira mfumu ya Turo ndipo uyiwuze mawu a Ine Ambuye
Yehova akuti,
“ ‘Iwe unali chitsanzo cha ungwiro weniweni,
wodzaza ndi nzeru ndi wokongola kwambiri.
13 Iwe unkakhala ngati mu Edeni,
munda wa Mulungu.
Miyala yokongola ya mitundu yonse:
rubi, topazi ndi dayimondi,
kirisoliti, onikisi, yasipa,
safiro, kalineliyoni ndi berili ndiwo inali zofunda zako.
Ndipo zoyikamo miyalayo zinali zagolide.
Anakupangira zonsezi pa tsiku limene unalengedwa.
14 Ndinayika kerubi kuti azikulondera.
Unkakhala pa phiri langa lopatulika,
ndipo unkayendayenda
pakati pa miyala ya moto.
15 Makhalidwe ako anali abwino
kuyambira pamene unalengedwa
mpaka nthawi imene unayamba kuchita zoyipa.
16 Unatanganidwa ndi zamalonda.
Zotsatira zake zinali zoti unachulukitsa zandewu
ndi kumachimwa.
Choncho ndinakuchotsa ku phiri langa lopatulika.
Mkerubi amene ankakulondera uja anakupirikitsa
kukuchotsa ku miyala yamoto.
17 Unkadzikuza mu mtima mwako
chifukwa cha kukongola kwako,
ndipo unayipitsa nzeru zako

chifukwa chofuna kutchuka.
Kotero Ine ndinakugwetsa pansi
kuti ukhala chenjezo pamaso pa mafumu.
18 Ndi malonda ako achinyengo unachulukitsa machimo ako.
Motero unayipitsa malo ako achipembedzo.
Choncho ndinabutsa moto pakati pako,
ndipo unakupsereza,
ndipo unasanduka phulusa pa dziko lapansi
pamaso pa anthu onse amene amakuona.
19 Anthu onse amitundu amene ankakudziwa
akuchita mantha chifukwa cha iwe.
Watheratu mochititsa mantha
ndipo sudzakhalaponso mpaka muyaya.' "

*Za Chilango cha Sidoni*

20 Yehova anandiyankhula nati: 21 "Iwe mwana wa munthu, utembe-
nukire ku mzinda wa Sidoni ndipo unenere mowudzudzula kuti, 22 'Ine
Ambuye Yehova ndikuti,
" 'Ndine mdani wako, iwe Sidoni,
ndipo ndidzalemekezedwa chifukwa cha iwe.
Anthu adzadziwa kuti Ine ndine Yehova
ndikadzakulanga ndi kudzionetsa kuti
ndine woyera pakati pako.
23 Ndidzatumiza mliri pa iwe
ndi kuchititsa magazi kuti ayende m'misewu yako.
Anthu ophedwa ndi lupanga
adzagwa mbali zonse.
Pamenepo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.
24 " 'Nthawi imeneyo Aisraeli sadzakhalanso ndi anthu pafupi
achipongwe amene ali ngati nthula zowawa ndi ngati minga zopweteka.
Pamenepo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Ambuye Yehova.
25 " 'Ine Ambuye Yehova mawu anga ndi awa: Nditasonkhanitsa Aisraeli
kuchoka ku mayiko kumene anamwazikira, ndidzadzionetsa kuti ndine
woyera pakati pawo pamaso pa anthu a mitundu ina. Adzakhala m'dziko
lawo, limene ndinalipereka kwa mtumiki wanga Yakobo. 26 Adzakhala
kumeneko mwamtendere ndipo adzamanga nyumba ndi kulima minda ya
mpesa. Adzakhala kumeneko mwamtendere pamene ndidzalange anthu
oyandikana nawo, amene ankawanyoza. Motero iwo adzadziwa kuti Ine
ndine Yehova Mulungu wawo.' "

# 29

*Za Chilango cha Igupto*

1 Pa tsiku lakhumi ndi chiwiri la mwezi wakhumi, chaka chakhumi,
Yehova anandiyankhula kuti: 2 "Iwe mwana wa munthu, tembenukira
kwa Farao, mfumu ya Igupto, ndipo unenere modzudzula mfumuyo
pamodzi ndi dziko lake. 3 Uyiwuze mfumuyo kuti, 'Ine Ambuye Yehova
ndikuti,
" 'Ndine mdani wako, iwe Farao mfumu ya Igupto,
iwe ng'ona yayikulu yogona pakati pa mitsinje yako.
Umanena kuti, 'Mtsinje wa Nailo ndi wanga;
ndinadzipangira ndekha.'
4 Koma ndidzakukola ndi mbedza m'kamwa mwako
ndipo nsomba za m'mitsinje yako zidzakangamira ku mamba ako.

Tsono ndidzakutulutsa mu mtsinje mwakomo
pamodzi ndi nsomba zimene zakangamira ku mamba ako.
5 Ndidzakutaya ku chipululu,
iwe pamodzi ndi nsomba zonse za m'mitsinje yako.
Udzagwera pamtetete kuthengo
popanda munthu woti akutole kuti akayike maliro ako.
Ndidzakusandutsa chakudya
cha zirombo za pa dziko lapansi ndi mbalame za mlengalenga.
6 Motero aliyense amene amakhala mu Igupto adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.

" 'Iwe unakhala ngati ndodo yabango ku Aisraeli. 7 Pamene anakugwira
unathethekera m'manja mwawo ndi kucheka mapewa awo. Pamene
anakutsamira, unathyoka ndipo misana yawo inagwedezeka.

8 " 'N'chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti, ndikubweretsera
lupanga kuti lidzaphe anthu pamodzi ndi nyama zomwe. 9 Dziko la Igupto
lidzasanduka lopanda anthu. Pamenepo iwo adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.

" 'Popeza iwe unati, 'Mtsinje wa Nailo ndi wanga; ndinawupanga
ndine,' 10 n'chifukwa chake Ine ndikudana nawe pamodzi ndi mitsinje
yakoyo, ndipo ndidzasandutsa dziko la Igupto bwinja kuyambira chipululu
cha Migidoli mpaka ku mzinda wa Asiwani, kukafika ku malire a
Kusi. 11 Palibe phazi la munthu kapena la nyama limene lidzapondepo.
Kudzakhala kopanda anthu kwa zaka makumi anayi. 12 Ndidzasandutsa
dziko la Igupto kukhala chipululu ngati zipululu za mayiko ena. Kwa zaka
makumi anayi mizinda yakenso idzakhala yopasuka pakati pa mizinda
yopasuka. Ndipo ndidzathamangitsira Aigupto pakati pa mitundu ya
anthu ndi kuwabalalitsira m'mayiko.

13 " 'Komabe Ine Ambuye Yehova ndikuti: Pakutha pa zaka makumi
anayi ndidzasonkhanitsa Aigupto onse kuchokera ku mayiko amene
ndinawabalalitsirako. 14 Ndidzachotsa Aiguptowo ku ukapolo ndipo
ndidzawabwezera ku Patirosi kumene anachokera. Kumeneko iwo
adzakhala ufumu wotsika. 15 Udzakhala ufumu wotsika kwambiri ku-
pambana maufumu ena onse ndipo sudzadzitukumula pakati pa mitundu
ina. Ndidzawufowoketsa kwambiri kotero kuti sudzathanso kulamulira
mitundu ya anthu. 16 Aisraeli sadzadaliranso Aigupto. Koma kuti
chilango chawo chidzawakumbutsa tchimo lawo lija lofunafuna thandizo
kuchokera ku Igupto. Pamenepo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Ambuye
Yehova.' "

### *Mphotho ya Nebukadinezara*

17 Pa tsiku loyamba la mwezi woyamba, chaka cha 27, Yehova
anandiyankhula kuti: 18 "Iwe mwana wa munthu, kale Nebukadinezara
mfumu ya Babuloni inagwiritsa ntchito ankhondo ake kukathira nkhondo
mzinda wa Turo, mpaka munthu aliyense anachita dazi chifukwa cho-
senza katundu, ndipo ananyuka pa phewa. Komabe ngakhale iyeyo,
kapena gulu lake lankhondo sanaphulepo kanthu pa ntchito yonse imene
anayigwira polimbana ndi mzindawo. 19 N'chifukwa chake Ine Ambuye
Yehova ndikuti, Ine ndidzapereka Igupto kwa Nebukadinezara mfumu
ya Babuloni, ndipo iyo idzatenga chuma chake ndi kuchifunkha ngati
malipiro a gulu lake lankhondo. 20 Ndamupatsa Nebukadinezara Igupto

ngati mphotho ya kulimbika kwake chifukwa iyo ndi gulu lake lankhondo anandigwirira ntchito, akutero Ambuye Yehova.
21 "Pa nthawi imeneyo ndidzapereka mphamvu yatsopano pa Aisraeli, ndipo ndidzatsekula pakamwa pako, iwe, Ezekieli kuti uthe kuyankhula pakati pawo. Pamenepo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

# 30

*Za Kulangidwa kwa Igupto*

1 Yehova anandiyankhula kuti: 2 "Iwe mwana wa munthu, nenera ndipo
ulengeze zimene Ine Ambuye Yehova ndikunena.

" 'Ufuwule mawu awa akuti,
'Kalanga, tsiku lafika!'
3 Pakuti tsiku layandikira,
tsiku la Yehova lili pafupi,
tsiku la mitambo yakuda,
tsiku lachiwonongeko cha mitundu ya anthu.
4 Lupanga lidzabwera kudzalimbana ndi Igupto
ndipo mavuto adzafika pa Kusi.
Pamene anthu ambiri adzaphedwa mu Igupto,
chuma chake chidzatengedwa
ndipo maziko ake adzagumuka.
5 Kusi, Puti, Ludi ndi Arabiya yense, Libiya ndiponso anthu a m'dziko logwirizana naye adzaphedwa ndi lupanga pamodzi ndi Igupto.

6 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti:
" 'Onse othandiza Igupto adzaphedwa
ndipo kunyadira mphamvu zake kudzatheratu.
Adzaphedwa ndi lupanga
kuyambira ku Migidoli mpaka ku mzinda wa Asiwani,' "
ndikutero Ine Ambuye Yehova.
7 " 'Dziko la Igupto lidzasanduka bwinja
kupambana mabwinja ena onse opasuka,
ndipo mizinda yake idzakhala yopasuka
kupambana mizinda ina yonse.
8 Nditatha kutentha Igupto
ndi kupha onse omuthandiza,
pamenepo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

9 " 'Nthawi imeneyo ikadzafika, amithenga adzapita mofulumira kuchokera kwa Ine kukaopseza Kusi, iwowo osadziwako kanthu. Ndipo adzada nkhawa pa tsiku limene Igupto adzawonongedwa, chifukwa tsikulo lidzafika ndithu.

10 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti,
" 'Ndidzagwiritsa ntchito Nebukadinezara, mfumu ya ku Babuloni
kuti ndithetse gulu lankhondo la Igupto.
11 Iye ndi gulu lake lankhondo, mtundu wa anthu ankhanza kwambiri aja
adzabwera kudzawononga dzikolo.
Adzasolola malupanga awo kulimbana ndi Igupto
ndipo dziko lidzadzaza ndi mitembo.
12 Ndidzawumitsa mtsinje wa Nailo
ndi kugulitsa dziko la Igupto kwa anthu oyipa.
Ndidzagwiritsa ntchito anthu achilendo kuti ndiwononge dzikolo
pamodzi ndi zonse zili m'menemo.

Ine Yehova ndayankhula.

13 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti,
" 'Ndidzawononga mafano
ndi kuthetsa milungu yosema ya ku Mefisi.
Simudzakhalanso mfumu mu Igupto,
ndipo ndidzaopseza dziko lonse.
14 Ndidzasandutsa chipululu mzinda wa Patirosi,
ndi kutentha mzinda wa Zowani.
Ndidzalanga mzinda wa Thebesi.
15 Ndidzakhuthulira ukali wanga pa mzinda wa Peluziumu,
linga lolimba la Igupto,
ndi kuwononga gulu lankhondo la Thebesi.
16 Ndidzatentha ndi moto dziko la Igupto;
Peluziumu adzazunzika ndi ululu.
Malinga a Thebesi adzagumuka,
ndipo mzindawo udzasefukira ndi madzi.
17 Anyamata a ku Oni ndi ku Pibeseti
adzaphedwa ndi lupanga
ndipo okhala m'mizinda yake adzatengedwa ukapolo.
18 Ku Tehafinehezi kudzakhala mdima
pamene ndidzathyola goli la Igupto;
motero kunyada kwake kudzatha.
Iye adzaphimbidwa ndi mitambo yakuda,
ndipo okhala m'mizinda yake adzapita ku ukapolo.
19 Kotero ndidzalanga dziko la Igupto,
ndipo iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.' "

### *Farao Watha Mphamvu*

20 Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri la mwezi woyamba wa chaka chakhumi
ndi chimodzi, Yehova anandiyankhula kuti: 21 "Iwe mwana wa munthu,
ndathyola dzanja la Farao mfumu ya Igupto. Taona, silinamangidwe kuti
lipole, ngakhale kulilimbitsa ndi nsalu kuti lithe kugwiranso lupanga.
22 N'chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti, Ine ndikudana ndi Farao
mfumu ya Igupto. Ndidzathyola manja ake onse; dzanja labwino pamodzi
ndi lothyokalo, ndipo lupanga lidzagwa m'manja mwake. 23 Ndidzamwaza
Aigupto pakati pa mitundu ya anthu ndikuwabalalitsira ku mayiko ambiri.
24 Ndidzalimbitsa manja a mfumu ya ku Babuloni, ndipo m'manja mwake
ndidzayikamo lupanga langa. Koma ndidzathyola manja a Farao, ndipo
adzabuwula ngati wolasidwa koopsa pamaso pa mfumu ya ku Babuloniyo.
25 Ndidzalimbitsa manja a mfumu ya ku Babuloni, koma manja a
Farao adzafowoka. Motero anthu adzadziwa kuti Ine ndine Yehova,
ndikadzayika lupanga langa m'manja mwa mfumu ya ku Babuloni. Ndipo
adzaligwiritsa ntchito pothira nkhondo dziko la Igupto. 26 Ndidzamwaza
Aigupto pakati pa mitundu ya anthu, ndikuwabalalitsira ku mayiko
ambiri. Motero adzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

## 31

### *Mkungudza mu Lebanoni*

1 Pa tsiku loyamba la mwezi wachitatu, chaka cha khumi ndi chimodzi,
Yehova anandiyankhula kuti: 2 "Iwe mwana wa munthu, unene kwa Farao
mfumu ya Igupto ndi gulu lake lankhondo. Awawuze kuti,
" 'Kodi mu ukulu wanu ndani angafanane ndi inu?
3 Taonani, ndidzakufanizirani ndi mtengo wa mkungudza wa ku Lebanoni,
wa nthambi zokongola zochititsa mthunzi m'nkhalango.
Unali wautali,
msonga zake zooneka pamwamba pa nkhalango.
4 Madzi ndiwo ankawukulitsa mkungudzawo,
akasupe ozama ankawutalikitsa.
Mitsinje yake inkayenda
mozungulira malo amene unaliwo
ndipo ngalande zake zinkafika
ku mitengo yonse ya m'munda.
5 Choncho unatalika kwambiri
kupambana mitengo yonse ya m'munda.
Nthambi zake zinachuluka
ndi kutalika kwambiri,
chifukwa inkalandira madzi ambiri.
6 Mbalame zonse zamlengalenga
zinkamanga zisa zake m'nthambi za mtengowo.
Nyama zakuthengo zonse
zinkaswanirana m'munsi mwa nthambi zake.
Mitundu yotchuka ya anthu
inkakhala mu mthunzi wake.
7 Unali wokongola kwambiri,
wa nthambi zake zotambalala,
chifukwa mizu yake inazama pansi
kumene kunali madzi ochuluka.
8 M'munda wa Mulungu munalibe
mkungudza wofanana nawo,
kapena mitengo ya payini
ya nthambi zofanafana ndi nthambi zake.
Munalibenso mtengo wa mkuyu
nthambi zofanafana ndi zake.
M'munda wa Mulungu munalibe mtengo wina uliwonse
wofanana ndi iwo kukongola kwake.
9 Ine ndinawupanga wokongola
wa nthambi zochuluka.
Mitengo yonse ya mu Edeni, m'munda wa
Mulungu inawuchitira nsanje.

10 " 'N'chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: Chifukwa kuti
mtengowo unatalika kwambiri, unatulutsa songa zake mpaka ku thambo,
ndipo unadzikweza chifukwa cha msinkhu wake, 11 ndinawupereka
m'dzanja la mfumu ya mitundu ya anthu kuti awulange molingana ndi
kuyipa kwake. 12 Anthu ankhanza kwambiri amitundu ya anthu achilendo
adzawudula ndi kuwusiya. Nthambi zake zidzagwera pa mapiri ndi mu
zigwa zonse. Nthambi zake zidzathyokera m'mitsinje ya m'dzikomo.
Motero mitundu yonse ya anthu a dziko lapansi amene ankasangalala mu
mthunzi wake idzawusiya. 13 Mbalame zonse zamlengalenga zidzakhala
pa mtengo wakugwawo, ndipo nyama zakuthengo zonse zidzakhala pa
nthambi zake. 14 Zidzakutero kuti pasakhalenso mitengo inanso ya

m’mbali mwa madzi yotalika kwambiri, imene idzatalike kwambiri ndi
songa zake kufika mpaka ku mitambo. Komanso kuti pasadzakhalenso
mitengo yolandira bwino madzi, imene idzatalika motero. Paja yonseyo
kutha kwake ndi kufa, kupita ku dziko lapansi kukhala ndi anthu akufa
amene analowa m’manda kale.
15 “ ‘Ine Ambuye Yehova ndikuti: Pa nthawi imene mkungudzawo
unatsikira ku manda, ndinawuza nyanja kuti iwulire maliro
pakuwuphimba. Ndinawumitsa mitsinje ndipo madzi ambiri anaphwa.
Ndinabweretsa mdima pa Lebanoni chifukwa cha mtengowo ndipo
mitengo yonse ya m’dzikomo inawuma. 16 Mitundu ya anthu
inagwedezeka pakumva mkokomo wa kugwa kwake, pamene
ndinawutsitsira ku manda pamodzi ndi iwo amene anafa. Pamenepo
ku dziko la akufa mitengo yonse ya ku Edeni pamodzi ndi ya ku Lebanoni
yosankhidwa bwino inasangalatsidwa chifukwa cha zimenezi. 17 Amene
ankakhala mu mthunzi wake, amene ankayanjana nawo, iwonso anapita
nawo pamodzi ku manda, kukakhala pamodzi ndi amene anaphedwa ndi
lupanga pakati pa mitundu ya anthu.
18 “ ‘Ndi mitengo iti ya mu Edeni imene ingafanane ndi kukongola kwako
ndi ulemerero wako? Komabe iwenso, udzatsikira ku dziko la anthu akufa
pamodzi ndi mitengo ya mu Edeni. Udzagona pamodzi ndi anthu osachita
mdulidwe, anthu amene anaphedwa pa nkhondo.

“ ‘Mtengowo ndi Farao ndi gulu lake lankhondo, akutero Ambuye
Yehova.’ ”

# 32

*Nyimbo ya Maliro a Farao*

1 Pa tsiku loyamba la mwezi wa khumi ndi chiwiri, chaka chakhumi ndi
chiwiri, Yehova anandiyankhula kuti: 2 “Iwe mwana wa munthu imba
nyimbo ya maliro a Farao mfumu ya Igupto ndipo uyiwuze kuti,

“Iwe umadziyesa ngati mkango pakati pa mitundu ya anthu.
    Koma iwe uli ngati ng’ona m’nyanja.
Umakhuvula m’mitsinje yako,
    kuvundula madzi ndi mapazi ako
    ndi kudetsa madzi m’mitsinje.

3 “Tsono Ine Ambuye Yehova ndikuti,

“ ‘Pogwiritsa ntchito gulu la anthu a mitundu yambiri,
    ndidzakuponyera khoka langa
    ndi kukugwira mu ukonde wanga.
4 Ndidzakuponya ku mtunda
    ndi kukutayira pansi.
Ndidzabweretsa mbalame zamumlengalenga kuti zidzatere pa iwe,
    ndipo zirombo zonse za dziko lapansi zidzakudya.
5 Ndidzayanika mnofu wako pa mapiri
    ndipo zigwa zidzadzaza ndi zotsalira zako.
6 Ndidzanyowetsa dziko ndi magazi ako,
    mpaka kumapiri komwe,
    ndipo mitsinje idzadzaza ndi mnofu wako.
7 Ndikadzakuwononga, ndidzaphimba miyamba
    ndikudetsa nyenyezi zake.
Ndidzaphimba dzuwa ndi mtambo,
    ndipo mwezi sudzawala.
8 Zowala zonse zamumlengalenga

ndidzazizimitsa;
ndidzachititsa mdima pa dziko lako,
akutero Ambuye Yehova.
9 Ndidzasautsa mitima ya anthu a mitundu yambiri
pamene ndidzakupititsa ku ukapolo pakati pa mitundu ya anthu,
ku mayiko amene iwe sunawadziwe.
10 Ine ndidzachititsa kuti anthu a mitundu yambiri adabwe nawe,
ndipo mafumu awo adzanjenjemera ndi mantha aakulu chifukwa cha iwe
pamene ndidzaonetsa lupanga langa pamaso pawo.
Pa nthawi ya kugwa kwako,
aliyense wa iwo adzanjenjemera
moyo wake wonse.
11 " 'Pakuti ndikunena Ine Ambuye Yehova kuti,
" 'Lupanga la mfumu ya ku Babuloni
lidzabwera kudzalimbana nawe.
12 Ndidzachititsa gulu lako lankhondo kuti ligwe
ndi lupanga la anthu amphamvu,
anthu ankhanza kwambiri pakati pa mitundu yonse ya anthu.
Adzathetsa kunyada kwa Igupto,
ndipo gulu lake lonse la nkhondo lidzagonjetsedwa.
13 Ndidzawononga ziweto zake zonse
zokhala m'mbali mwa madzi ambiri.
Ku madziko sikudzaonekanso phazi la munthu
kapena kudetsedwa ndi phazi la ziweto.
14 Pambuyo pake ndidzayeretsa madzi ake
ndipo mitsinje yake idzayenda mokometsera ngati mafuta,
akutero Ambuye Yehova.
15 Ndikadzasandutsa dziko la Igupto kukhala bwinja;
ndikadzawononga dziko lonse
ndi kukantha onse okhala kumeneko,
adzadziwa kuti ndine Yehova.'
16 "Mawu angawa adzakhala nyimbo ya maliro. Ana a akazi amitundu
ya anthu adzayimba, kuyimbira Igupto ndi gulu lake lonse la nkhondo,
akutero Ambuye Yehova."

17 Pa tsiku la 15 la mwezi woyamba, chaka cha khumi ndi chiwiri, Yehova
anayankhula kuti: 18 "Iwe mwana wa munthu, lirira gulu lankhondo la
Igupto ndipo uwalowetse pamodzi ndi anthu ena amphamvu a mayiko
ena ku dziko la anthu akufa. 19 Ufunse kuti, 'Ndani amene akukuposa
kukongola? Tsikirani ku manda ndi kukhala pamodzi ndi anthu osachita
mdulidwe.' 20 Aigupto adzagwa pakati pa amene akuphedwa ndi lupanga.
Lupanga ndi losololedwa kale. Iye adzaphedwa pamodzi ndi gulu lake
lankhondo. 21 M'kati mwa manda atsogoleri amphamvu pamodzi ndi
ogwirizana nawo azidzakambirana za Igupto n'kumati, 'Afika kuno anthu
osachita mdulidwe aja! Ndi awa agona apawa, ophedwa pa nkhondo.'
22 "Asiriya ali komweko ndipo ankhondo ake onse ali m'manda
omuzungulira. Onsewo anaphedwa pa nkhondo. 23 Manda awo ali kumalo
ozama a dzenje, ndipo ankhondo ake azungulira manda ake. Onse amene
anaopseza dziko la anthu amoyo aphedwa, agwa ndi lupanga.
24 "Elamu ali komweko ndipo ankhondo ake ali m'manda omuzun-
gulira. Onsewa anaphedwa pa nkhondo, natsikira ku manda ali osachita

mdulidwe. Iwowa kale ankaopseza anthu pa dziko lapansi. Tsopano
akuchita manyazi pamodzi ndi amene ali m'manda. 25 Amukonzera
pogona pakati pa anthu ophedwa, pamodzi ndi gulu lake lonse la nkhondo
litazungulira manda ake. Onsewo ndi anthu osachita mdulidwe ophedwa
ndi lupanga. Paja anthuwa ankaopsa m'dziko la anthu a moyo. Koma
tsopano akuchita manyazi pamodzi ndi amene ali m'manda. Iwo ayikidwa
pakati pa anthu ophedwa.

26 "Mesaki ndi Tubala ali komweko, pamodzi ndi gulu lonse la nkhondo
litazungulira manda awo. Onsewo ndi anthu osachita mdulidwe, ophedwa
ndi lupanga. Paja ankaopsa m'dziko la anthu amoyo. 27 Iwo sanayikidwe
mwaulemu ngati ankhondo amphamvu amakedzana, amene anatsikira ku
dziko la anthu akufa ndi zida zawo zomwe za nkhondo. Malupanga awo
anawayika ku mitu yawo, ndipo zishango zawo anaphimba mafupa awo.
Kale anthu amphamvu amenewa ankaopsa dziko la anthu amoyo.

28 "Iwenso Farao, udzaphwanyidwa ndi kuyikidwa pakati pa anthu
osachita mdulidwe, amene anaphedwa ndi lupanga.

29 "Edomu ali kumeneko pamodzi ndi mafumu ake ndi akalonga ake
onse. Ngakhale anali amphamvu, koma anayikidwa. Ayikidwa pamodzi
ndi anthu osachita mdulidwe, pamodzi ndi iwo amene akutsikira ku
dzenje.

30 "Akalonga onse akumpoto pamodzi ndi anthu onse a ku Sidoni ali
kumeneko. Anatsikira ku dziko la anthu akufa mwamanyazi ngakhale
anali owopsa ndi mphamvu zawo. Iwo akugona osachita mdulidwe
pamodzi ndi amene anaphedwa ndi lupanga ndipo akuchita manyazi
pamodzi ndi iwo amene anatsikira kale ku manda.

31 "Farao ndi gulu lake lankhondo akadzawaona iwowa adzathunza
mtima pokumbukira kuchuluka kwa gulu lake lankhondo limene
linaphedwa pa nkhondo. Ndikutero Ine Ambuye Yehova. 32 Paja ankaopsa
m'dziko la anthu amoyo. Koma Faraoyo pamodzi ndi ankhondo ake onse
adzayikidwa pamodzi ndi anthu osachita mdulidwe, pamodzi ndi amene
anaphedwa pa nkhondo. Ndikutero Ine Ambuye Yehova."

# 33

*Ezekieli Akhala Mlonda*

1 Yehova anandiyankhula nati: 2 "Iwe mwana wa munthu awuze anthu
a mtundu wako kuti, 'Paja zimati ndikatumiza nkhondo m'dziko anthu a
m'dzikomo amasankha munthu mmodzi pakati pawo kuti akhale mlonda.
3 Tsono iyeyo amati akaona nkhondo ikubwera amaliza lipenga kuti
achenjeze anthuwo. 4 Wina aliyense akamva lipenga koma osasamala,
mdani uja akabwera n'kumupha, ndiye kuti wadziphetsa yekha. 5 Iye
anamva kulira kwa lipenga koma sanalabadire. Ndiye kuti wadziphetsa
yekha. Akanasamala kuchenjeza kwa mlonda akanapulumuka. 6 Koma
ngati mlondayo aona lupanga likubwera ndipo osawomba lipengalo
kuchenjeza anthu, ndipo lupanga libwera ndi kuchotsa moyo wa mmodzi
mwa iwo, munthu ameneyo adzafa chifukwa cha tchimo lake, koma
ndidzamuyimba mlandu mlondayo chifukwa cha imfa ya mnzakeyo.'

7 "Tsono iwe mwana wa munthu, ndakuyika kuti ukhale mlonda wa
Aisraeli. Choncho imva mawu amene ndikuyankhula ndipo uwachenjeze.
8 Ndikawuza munthu woyipa kuti, 'Iwe munthu woyipa, udzafa ndithu,'
ndipo iwe osayankhula kumuchenjeza kuti aleke njira zake, munthu
wochimwayo adzafa chifukwa cha tchimo lake, koma Ine ndidzakuyimba

mlandu chifukwa cha imfa yake. [9] Koma ngati uchenjeza munthu woyipa
kuti aleke njira zake, ndipo iye osatero, adzafa chifukwa cha tchimo lake,
koma iwe udzapulumutsa moyo wako.

[10] "Iwe mwana wa munthu, akumbutse Aisraeli mawu awo akuti,
'Ife talemedwa ndi zolakwa zathu ndi machimo athu, ndipo tikuwonda
chifukwa cha zimene tachita. Kodi tingakhale ndi moyo bwanji?' "
[11] Uwawuze kuti, Ine Ambuye Yehova ndikuti: "Pali Ine wamoyo,
sindikondwera ndi imfa ya munthu woyipa. Ndimakondwera ndikamaona
munthu woyipa akuleka zoyipa zake kuti akhale ndi moyo. Tembenukani!
Tembenukani, siyani makhalidwe anu oyipa! Muferanji, Inu Aisraeli?

[12] "Tsono iwe mwana wa munthu, awuze anthu a mtundu wako
kuti, 'Ngati munthu wolungama achimwa, ndiye kuti ntchito zake
zabwino zija sizidzamupulutsa. Koma wochimwa akaleka ntchito zake
zoyipazo, sadzalangidwa konse. Ndithu ngati munthu wolungama ayamba
kuchimwa sadzatha kukhala ndi moyo chifukwa cha ntchito zake zabwino
zija.' [13] Ngati ndiwuza munthu wolungama kuti adzafa ndithu, koma
iyeyo n'kumadalira ntchito zake zabwino zimene anachita kale ndi
kuyamba kuchimwa, ndiye kuti ntchito zake zabwinozo zidzayiwalika.
Iye adzafa chifukwa cha machimo ake. [14] Ndipo ngati ndiwuza munthu
woyipa kuti, 'Udzafa ndithu,' tsono iye n'kutembenuka kuleka machimo
ake ndi kuyamba kuchita zimene Yehova afuna, [15] monga kubweza
chimene anatenga ngati chikole cha ngongole, kubweza chimene anaba,
kutsatira malamulo omwe amapereka moyo ndi kuleka kuchita zoyipa,
iye adzakhala ndithu ndi moyo; sadzafa. [16] Ndidzakhululuka machimo
ake onse anachita. Iye wachita zimene ndi zolungama ndi zoyenera ndipo
iye adzakhala ndi moyo ndithu.

[17] "Komabe anthu a mtundu wako akunena kuti, 'Zimene Ambuye
amachita ndi zopanda chilungamo.' Ayi, koma makhalidwe awo ndiwo ali
osalungama. [18] Ngati munthu wolungama atembenuka ndi kuleka ntchito
zake zolungama ndi kuyamba kuchita zoyipa, adzafa nazo. [19] Ndipo
ngati munthu woyipa atembenuka ndi kuleka ntchito zake zoyipa ndi
kuyamba kuchita zolungama ndi zoyenera, iye adzakhala ndi moyo
pochita zimenezo. [20] Koma Inu Aisraeli, mukunena kuti, 'Zimene Ambuye
amachita ndi zopanda chilungamo.' Ayi, inu Aisraeli, Ine ndidzaweruza
aliyense wa inu potsata ntchito zake."

### *Mbiri ya Kuwonongeka kwa Yerusalemu*

[21] Pa tsiku lachisanu la mwezi wakhumi, chaka chakhumi ndi chiwiri
cha ukapolo wathu, munthu wina amene anapulumuka ku Yerusalemu
anabwera kudzandiwuza kuti, "Mzinda wagwa!" [22] Tsono madzulo ake
munthuyo asanafike, dzanja la Yehova linali pa ine. Koma mmawa mwake
munthuyo atabwera Yehova anatsekula pakamwa panga, motero kuti
sindinakhalenso wosayankhula.

[23] Ndipo Yehova anandiyankhula kuti: [24] "Iwe mwana wa munthu, an-
thu amene akukhala m'mizinda ya mabwinja ya dziko la Israeli akunena
kuti, 'Abrahamu anali munthu mmodzi yekha, ndipo anamupatsa dziko
lonse. Koma ife tilipo ambiri, motero tsono dzikolo ndi lathu.' [25] Choncho
iwe uwawuze kuti Ine Ambuye Yehova ndikuti, 'Inu mumadya nyama ili
ndi magazi ake, ndipo mumapembedza mafano ndi kukhetsa magazi, kodi
tsono inu n'kulandira dzikoli? [26] Mumadalira lupanga lanu, mumachita
zinthu zonyansa, ndipo aliyense wa inu amachita chigololo ndi mkazi wa
mnzake. Kodi inu n'kulandira dzikoli?'

27 “Uwawuze kuti Ine Ambuye Yehova ndikuti, ‘Ndithu pali Ine wamoyo,
anthu amene anatsala m'mizinda ya mabwinja adzaphedwa ndi lupanga,
amene ali ku midzi ndidzawapereka kuti adzadyedwe ndi zirombo
zakuthengo, ndipo amene ali m'malinga ndi m'mapanga adzafa ndi
mliri. 28 Ndidzalisandutsa chipululu dzikolo, ndipo mphamvu zake zimene
amanyadira zidzatheratu, ndipo mapiri a Yerusalemu adzasanduka chip-
ululu, kotero kuti palibe amene adzatha kudutsako. 29 Ndikadzasandutsa
dzikolo chipululu chifukwa cha zonyansa zimene ankachita, pamenepo
ndiye adzadziwa kuti ndine Yehova.’

30 “Koma kunena za iwe, mwana wa munthu, anthu a mtundu wako
akumayankhula za iwe akakhala pa makoma a mzinda ndi pa makomo
a nyumba zawo. Akumawuzana kuti, ‘Tiyeni tikamve uthenga umene
wachokera kwa Yehova.’ 31 Anthu anga amabwera kwa iwe, monga
momwe amachitira nthawi zonse anthu anga, ndipo amakhala pansi
pamaso pako kumvetsera mawu ako. Koma zimene akumvazo sazichita.
Zokamba zawo zimaonetsa chikondi, koma mitima yawo imakhala pa
phindu lawo. 32 Kunena zoona, kwa iwowo sindiwe kanthu konse,
ndiwe munthu wamba chabe womangoyimba nyimbo zachikondi ndi liwu
lokoma poyimba zeze. Kumva amamva mawu ako koma sawagwiritsa
ntchito.

33 “Koma zonsezi zikadzachitika, ndipo zidzachitika ndithu, pamenepo
adzadziwa kuti mneneri anali pakati pawo.”

# 34

*Abusa a Israeli*

1 Yehova anandiyankhula kuti: 2 “Iwe mwana wa munthu, yankhula
mawu oyimba mlandu abusa a Israeli. Lengeza ndipo uwawuze kuti
Ine Ambuye Yehova ndikuti, ‘Tsoka kwa abusa a Israeli amene muman-
godzisamala nokha! Kodi abusa sayenera kusamalira nkhosa? 3 Mumadya
chambiko, mumadziveka zovala zaubweya, ndi kupha nyama zonenepa,
koma simusamalira nkhosazo. 4 Simunalimbitse nkhosa zofowoka,
kapena kuchiritsa zodwala, kapena kumanga mabala a nkhosa zopweteka.
Simunabweze zosochera kapena kufunafuna zotayika. Munaziweta
mozunza ndi mwankhanza. 5 Kotero zinabalalika chifukwa zinalibe
m'busa, ndipo pamene zinabalalika zinakhala chakudya cha zirombo
zonse zakuthengo. 6 Nkhosa zanga zinayendayenda m'mapiri onse ndi
m'zitunda zonse zazitali. Zinabalalika pa dziko lonse lapansi, ndipo palibe
amene anazilondola kapena kuzifunafuna.

7 “ ‘Choncho Inu abusa, tamvani zimene Ine Yehova ndikukuwuzani.
8 Pali Ine wamoyo, akutero Ambuye Wamphamvuzonse, ndithu, nkhosa
zanga zinajiwa ndi zirombo zakuthengo, zinasanduka chakudya cha
zirombo chifukwa panalibe abusa. Abusa anga sanafunefune nkhosa
zanga. Iwo ankangosamala za iwo okha m'malo mosamala nkhosa
zanga. 9 Chifukwa chake, inu abusa, tamvani zimene Ine Yehova
ndikukuwuzani. 10 Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ine ndayipidwa nanu,
inu abusa. Ndidzakulandani nkhosa zanga ndipo simudzazidyetsanso.
Ndidzakuchotsani pa ntchito ya ubusa kuti musamangodzidyetsa nokha.
Ndidzalanditsa nkhosa zanga kukamwa kwanu ndipo simudzazidyanso.

11 “ ‘Tsono Ine Ambuye Yehova ndikuti, mwini wakene ndidzazifunafuna
nkhosa zanga ndi kuzisamalira. 12 Monga m'busa amanka nafunafuna

nkhosa zake pamene zina zabalalikira kutali, moteronso Ine ndidzafuna-
funa nkhosa zanga. Ndidzazipulumutsa kuchoka kumalo onse kumene
zinabalalikira pa nthawi yankhungu ndi mdima. 13 Ndidzazitulutsa pakati
pa mitundu ya anthu ndi kuzisonkhanitsa kuchokera ku mayiko ena,
ndipo ndidzazibwezera ku dziko lawo. Ndidzaziwetera ku mapiri a
Israeli, m'mbali mwa mitsinje ndi kumalo kumene kumakhala anthu.
14 Ndidzaziwetera kumalo a msipu wabwino. Mapiri okwera a Israeli
adzakhala malo azidyetserako. Kumeneko zidzapumula ku abusa abwino
a msipu ndipo zizidzadyadi msipu wonenepetsa pa mapiri a Israeli.
15 Ine mwini wake ndidzaziweta nkhosa zanga ndi kuzilola kuti zipumule.
Ndikutero Ine Ambuye Yehova. 16 Ndidzafunafuna zotayika ndi kubweza
zosochera. Ndidzamanga mabala a zopweteka ndi kulimbikitsa zofowoka.
Koma zonenepa ndi zamphamvu ndidzaziwononga. Ndidzaweta nkhosazo
mwachilungamo.

17 " 'Kunena za inu, nkhosa zanga, Ine Ambuye Yehova ndikuti:
Ndidzaweruza pakati pa nkhosa ndi nkhosa, pakati pa nkhosa zaz-
imuna ndi mbuzi zazimuna. 18 Kodi sikukukwaniranani kudya msipu
wabwino kuti muzichita kuponderezanso msipu umene simunadyewo?
Kodi simukhutira ndi kumwa madzi abwino kuti muzinka mudetsanso
madzi otsalawo ndi mapazi anu? 19 Kodi nkhosa zanga zidye zimene
mwazipondaponda ndi kumwa madzi amene mwawadetsa ndi mapazi
anu?

20 " 'N'chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: Taonani, Ine
mwini wake ndidzaweruza pakati pa nkhosa zonenepa ndi nkhosa
zowonda. 21 Popeza zofowoka mumaziwomba ndi kuzikankhira kumbali,
ndipo mumazigunda ndi nyanga zanu n'kuzimwazira kutali, 22 tsono
Ine ndidzapulumutsa nkhosa zanga, ndipo sindidzalolanso kuti zijiwe.
Ndidzaweruza pakati pa nkhosa ina ndi nkhosa inanso. 23 Ndidzaziyikira
m'busa mmodzi, mtumiki wanga Davide. Iyeyo ndiye azidzazisamala.
Adzakhala m'busa wawo. 24 Ine Yehova ndidzakhala Mulungu wake ndipo
mtumiki wanga Davide adzakhala mfumu pakati pa nkhosazo. Ine Yehova
ndayankhula.

25 " 'Ndidzapangana nazo pangano la mtendere. Ndidzachotsa
m'dzikomo zirombo zolusa. Choncho nkhosa zanga zidzakhala mu
mtendere mu chipululu ngakhalenso m'thengo. 26 Ndidzakhazika anthu
anga pafupi ndi phiri langa loyera ndipo ndidzawadalitsa. Ndidzawag-
wetsera mvula pa nthawi yake ndipo idzakhala mvula ya madalitso.
27 Mitengo ya m'minda idzabereka zipatso zake, ndipo nthaka idzakhala
ndi zokolola zake. Anthu adzakhala mwamtendere m'dziko lawo.
Iwo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, pamene ndidzathyola magoli
awo ndi kuwapulumutsa kuchoka m'manja mwa amene anawagwira
ukapolo. 28 Anthu amitundu ina sadzawafunkhanso ndipo sadzadyedwa
ndi zirombo zakuthengo. Adzakhala mwamtendere ndipo palibe amene
adzawaopseze. 29 Ndidzawapatsa zokolola zochuluka motero kuti sadza-
vutikanso ndi njala. Anthu a mitundu ina sadzawanyozanso. 30 Pamenepo
iwo adzadziwa kuti Ine Yehova Mulungu wawo ndili nawo pamodzi, ndipo
kuti iwo, Aisraeli, ndi anthu anga. Ndikutero Ine Ambuye Yehova. 31 Inu
ndinu nkhosa zanga, nkhosa zimene ndimazidyetsa. Ine ndine Mulungu
wanu. Ndikutero Ine Ambuye Wamphamvuzonse.' "

## 35

*Za Chilango cha Edomu*

1 Yehova anandiyankhula kuti: 2 "Iwe mwana wa munthu, yang'ana
phiri la Seiri; yankhula moliyimba mlandu ndipo 3 awawuze anthu
a kumeneko kuti zimene ndikuyankhula Ine Ambuye Yehova ndi izi:
Inu anthu a ku mapiri a Seiri ndikudana nanu. Ndidzatambasula
dzanja langa kulimbana nanu, ndipo ndidzasandutsa dziko lanu kukhala
chipululu. 4 Mizinda yanu ndidzayisandutsa mabwinja, ndipo dziko lanu
lidzasanduka chipululu. Zikadzachitika izi mudzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.
5 "Munali adani a Israeli nthawi zonse, ndipo munkalola kuti Aisraeli
aphedwe pa nkhondo pa nthawi ya mavuto awo, pa nthawi imene
chilango chawo chinafika pachimake. 6 N'chifukwa chake Ine Ambuye
Yehova ndikuti: Pali Ine wamoyo, ndithu ndidzakukanthani. Imfa
idzakulondolani. Popeza sunadane nako kukhetsa magazi, imfa idza-
kulondola. 7 Phiri la Seiri ndidzalisandutsa chipululu ndipo ndidzapha
onse amene amapita nabwerera kumeneko. 8 Ndidzaza mapiri ake ndi
mitembo. Ophedwa pa nkhondo adzagwera pa zitunda zanu, zigwa
zanu ndi m'mitsinje yanu yonse. 9 Ndidzasandutsa dziko lanu kukhala
chipululu mpaka muyaya, ndipo m'mizinda yanu simudzakhalanso anthu.
Zikadzachitika izi mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.
10 "Inu munanena kuti, 'Mitundu iwiri iyi ya anthu, Yuda ndi Israeli,
pamodzi ndi mayiko awo omwe idzakhala yathu.' Munanena chomwechi
ngakhale kuti Ine Yehova ndinali momwemo. 11 N'chifukwa chake Ine
Ambuye Yehova ndikuti: Pali Ine wamoyo, ndithu ndidzachita nanu
monga munachita ndi anthu a ku Yuda ndi Israeli poonetsa mkwiyo wanu,
nsanje yanu ndi chidani chanu pa iwo. Ndikadzakulangani mudzandidzi-
wadi pakati panupo. 12 Ndipo mudzadziwa kuti Ine Yehova ndinamva
mawu anu onse onyoza amene munanena molimbana ndi mapiri a Israeli.
Inu munati, 'Mapiri a Israeli asanduka bwinja, ndipo aperekedwa kwa
ife kuti tiwawononge.' 13 Mawu anu amene munayankhula monyada
kundinyoza Ine ndinawamva. 14 Ine Ambuye Yehova ndikuti: Dziko lonse
lapansi lidzasangalala pamene ndidzakusandutsani bwinja. 15 Monga
momwe inu munasangalala pamene anthu anga Aisraeli anagwa, Inenso
ndidzakuchitani chimodzimodzi. Udzasanduka bwinja, iwe Phiri la Seiri,
iwe ndi dziko lonse la Edomu. Zikadzatero anthu onse adzadziwa kuti Ine
ndine Yehova."

# 36

*Kubwezeretsedwa kwa Israeli*

1 "Iwe mwana wa munthu, yankhula kwa mapiri a Israeli ndipo unene
kuti, 'Inu mapiri a Israeli, imvani mawu a Yehova.' 2 Ine Ambuye Yehova
ndikuti: Mdani wanu ankanena kuti, 'Aa! Dziko lamapiri lakalekale
lija lasanduka lathu.' 3 Choncho nenera ndipo uwawuze kuti, 'Ine
Ambuye Yehova ndikuti: Popeza anakusakazani ndi kukuponderezani
ku mbali zonse motero kuti munakhala m'manja mwa anthu a mitundu
ina yonse ndipo anthu ankakunenani ndi kukunyozani, 4 choncho, inu
mapiri a Israeli, imvani zimene Ine Ambuye Yehova ndikuwuza mapiri
ndi magomo, zigwembe ndi zigwa, mabwinja ndi mizinda yosiyidwa
imene yakhala ikufunkhidwa komanso kunyozedwa ndi anthu a mitundu
ina okuzungulirani. 5 Tsono Ine Ambuye Yehova ndikuti: Mu mkwiyo
wanga woopsa ndinayankhula kuyimba mlandu mitundu ina yonse ya
anthu makamaka a ku Edomu. Iwowa mwa chimwemwe chodzaza

tsaya ndi mwa nkhwidzi analanda dziko langa ndi kulisandutsa lawo ndi
kutengeratu dziko la msipu kukhala lawo.’ 6 N’chifukwa chake, lengeza
ku dziko la Israeli, ndipo uwuze mapiri ndi magomo, zigwembe ndi zigwa
kuti, ‘Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ine ndikuyankhula ndi mtima wokwiya
kwambiri chifukwa inu munalandira chitonzo cha anthu a mitundu ina.’
7 Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ndikulumbira nditakweza dzanja langa kuti
mitundu ya anthu idzatozedwanso.

8 “Koma Inu mapiri a Israeli mudzaphukanso nthambi ndipo mudza-
wabalira zipatso anthu anga a Israeli, pakuti ali pafupi kubwerera
kwawo. 9 Taonani, Ine ndili mbali yanu ndipo ndidzakukomerani mtima.
Mudzalimidwa ndi kudzalidwa. 10 Ndidzachulukitsa chiwerengero cha
anthu anu, nyumba yonse ya Israeli. M’mizinda mudzakhalanso anthu
ndipo mabwinja adzamangidwanso. 11 Ndidzachulukitsa chiwerengero
cha amuna pamodzi ndi ziweto zomwe, ndipo adzachuluka kwambiri ndi
kubereka ana ambiri. Ndidzakhazika anthu m’dzikomo monga analili
kale, ndi kukulemeretsani kuposa kale. Pamenepo inu mudzadziwa kuti
Ine ndine Yehova. 12 Ndidzachititsa anthu kuyenda pa inu, ndiye kuti inu
anthu anga Aisraeli. Iwowo adzakhazikika pa inu, ndipo inu mudzakhala
cholowa chawo. Simudzalandanso ana awo.

13 “Ine Ambuye Yehova ndikuti: Popeza anthu amanena kuti, ndiwe
dziko limene limadya anthu ake ‘kulanda ana a mtundu wake,’
14 n’chifukwa chake, simudzadyanso anthu kapena kulanda ana a mtundu
wako. Ine Ambuye Yehova ndikutero. 15 Sindidzakulolaninso kumva
mnyozo wa anthu a mitundu ina, kapena kupirira kunyogodola kwawo
kapenanso kupunthwitsanso anthu a m’dziko lako. Ndikutero Ine Ambuye
Yehova.”

16 Yehova anandiyankhulanso kuti: 17 “Iwe mwana wa munthu,
pamene anthu a Israeli ankakhala m’dziko lawolawo, analiyipitsa ndi
makhalidwe awo ndiponso zochita zawo. Machitidwe awo pamaso panga
anali onyansa pa zachipembedzo ngati msambo wa mkazi amene ali
pa nthawi yake. 18 Tsono ndinawalanga chifukwa cha magazi amene
anakhetsa m’dzikomo, ndiponso chifukwa anayipitsa dziko ndi mafano
awo. 19 Ndinawamwaza pakati pa anthu a mitundu ina ndipo anabal-
alikira m’mayiko onse. Ndinawalanga molingana ndi makhalidwe awo
ndi zochita zawo. 20 Atafika kwa anthu a mitundu ina, kulikonse kumene
anapitako, anayipitsa dzina langa loyera. Zinatero popeza anthu ponena
za iwo ankanena kuti, ‘Awa ndi anthu a Yehova, komatu anachotsedwa ku
dziko lake.’ 21 Koma Ine ndinkadera nkhawa dzina langa loyera, limene
Aisraeli analiyipitsa pakati pa anthu a mitundu ina kumene anapitako.

22 “N’chifukwa chake awuze Aisraeliwo kuti Ine Ambuye Yehova ndikuti:
Ine ndidzachita zimene ndidzachitezo osati chifukwa cha inuyo Aisraelinu
ayi, koma chifukwa cha dzina langa, limene mwaliyipitsa pakati pa anthu
a mitundu ina kumene munapitako. 23 Ndidzaonetsa chiyero cha dzina
langa lotchuka, limene layipitsidwa pakati pawo. Anthu a mitundu inayo
atadzazindikira kuti ndaonetsa kudzera mwa inu kuti dzina langa ndi
loyera, iwo adzadziwanso kuti Ine ndine Yehova. Ndikutero Ine Ambuye
Yehova.

24 “Pakuti Ine ndidzakuchotsani pakati pa anthu a mitundu ina.
Ndidzakusonkhanitsani kuchoka ku mayiko onse ndi kukubwezerani ku
dziko lanulanu. 25 Ndidzakuwazani madzi oyera, ndipo mudzakhala oyera
mtima. Zonse zimene zimakuyipitsani zidzachoka. Ndidzakuyeretsani
pochotsa mafano anu onse. 26 Ndidzakupatsani mtima watsopano ndi

kulowetsa mzimu watsopano mwa inu. Ndidzachotsa mwa inu mtima
wanu wowuma ngati mwala ndi kukupatsani mtima wofewa ngati
mnofu. [27] Ndipo ndidzayika Mzimu wanga mwa inu ndipo ndidza-
kuthandizani kutsatira malangizo anga ndi kukusungitsani mosamala
kwambiri malamulo anga. [28] Mudzakhala m'dziko limene ndinapatsa
makolo anu. Mudzakhala anthu anga, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu
wanu. [29] Ndidzakupulumutsani ku zonse zokuyipitsani. Ndidzakuchuluk-
itsirani tirigu ndipo sindidzakugwetseraninso njala. [30] Ndidzachulukitsa
zipatso za m'mitengo yanu ndi zokolola za m'munda mwanu, kotero kuti
simudzanyozedwanso pakati pa anthu a mitundu ina chifukwa cha njala.
[31] Pamenepo mudzakumbukira makhalidwe anu oyipa ndi ntchito zanu
zoyipa. Machimo anu ndi ntchito zanu zonyansa zidzakuchititsa nokha
manyazi. [32] Tsono dziwani kuti Ine sindidzachita zimenezi chifukwa
cha inuyo ayi, ndikutero Ine Ambuye Wamphamvuzonse. Ndiyetu
chitani manyazi ndipo mugwetse nkhope zanu, inu Aisraeli chifukwa cha
makhalidwe anu!

[33] "Ine Ambuye Yehova ndikuti: Pa tsiku limene ndidzayeretse machimo
anu onse, ndidzayikamonso anthu m'mizinda yanu, ndipo ndidzaman-
ganso nyumba pa mabwinja. [34] Dziko limene linasanduka chipululu
lizidzalimidwanso. M'malo moti aliyense wopitamo alione dzikolo ngati
chipululu tsopano adzaliona lolimidwa. [35] Iwo adzati, 'Dziko ili, limene
linali chipululu, lasanduka munda wa Edeni. Mizinda imene inali
mabwinja osiyidwa ndi owonongedwa, tsopano ndi yotetezedwa ndi
yokhalamo anthu. [36] Ndipo anthu a mitundu ina okhala pafupi nanu
amene anatsala adzadziwa kuti Ine Yehova ndine amene ndinamanganso
mizinda yowonongeka ndi kudzalanso zinthu zatsopano m'malo m'mene
munali chipululu. Ine Yehova ndayankhula ndipo ndidzazichitadi.'

[37] "Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ndidzalolanso Aisraeli kuti andipem-
phe zoti ndiwachitire: Ndidzachulukitsa anthu awo ngati nkhosa.
[38] Adzachulukadi ngati nkhosa zomwe ankapereka ngati nsembe ku
Yerusalemu pa nthawi za chikondwerero. Choncho mizinda ya mabwinja
idzadzaza ndi anthu. Zikadzatero adzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

# 37

*Chigwa cha Mafupa Owuma*

[1] Dzanja la Yehova linali pa ine, ndipo Mzimu wa Yehova unandinyamula
n'kukandikhazika pakati pa chigwa. Chigwacho chinali chodzaza ndi
mafupa. [2] Yehova anandiyendetsa uku ndi uku pakati pa mafupawo.
Mafupawo anali ochuluka kwambiri m'chigwa monsemo ndipo anali
owuma kwambiri. [3] Tsono Yehova anandifunsa kuti, "Iwe mwana wa
munthu, kodi mafupa amenewa angakhalenso ndi moyo?"

Ndinayankha kuti, "Inu Ambuye Yehova, Inuyo nokha ndiye
mukudziwa."

[4] Pamenepo anandiwuza kuti, "Lengeza kwa mafupa amenewa ndi
kuwawuza kuti amve mawu a Ine Yehova! [5] Uwawuze kuti zimene
Ine Ambuye Yehova ndikunena kwa mafupa ndi izi: Ndidzawuzira
mpweya mwa inu, ndipo mudzakhalanso ndi moyo. [6] Ndidzakupatsani
mitsempha ndi mnofu. Ndiponso ndidzakukutani ndi khungu. Pambuyo
pake ndidzawuzira mpweya mwa inu ndipo mudzakhalanso ndi moyo.
Pamenepo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova."

7 Ndipo ndinanenera monga anandilamulira. Ndipo pamene ndinkanen-
era, ndinamva gobedegobede, ndipo mafupa aja anayamba kulumikizana,
fupa ku fupa linzake. 8 Ine ndinayang'ana, ndipo mitsempha ndi mnofu
zinabwera pa mafupawo ndipo khungu linaphimba pamwamba pake,
koma munalibe mpweya mwa iwo.
9 Tsono Yehova anandiwuza kuti, "Nenera kwa mpweya, nenera iwe
mwana wa munthu ndi kuwuza mpweya mawu a Ine Ambuye Yehova
kuti, 'Bwera kuno iwe mpweya. Bwera kuchokera ku mbali zonse zinayi
ndi kudzawuzira anthu ophedwawa kuti akhalenso ndi moyo.' 10 Choncho
ndinanenera monga anandilamulira ndipo mpweya unalowa mwa iwo;
apo anthu akufawo anakhala ndi moyo, nayimirira ndipo linali gulu
lalikulu lankhondo."
11 Kenaka Yehova anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu, mafupa
awa ndi nyumba yonse ya Israeli. Iwo amanena kuti, 'Mafupa athu awuma
ndipo chiyembekezo chathu chatayika, ife tawonongeka!' 12 N'chifukwa
chake nenera ndi kuwawuza kuti, 'Ine Ambuye Yehova ndikuti: Inu
anthu anga, ndidzafukula manda anu, ndipo ndidzakutulutsanimo ndi
kukubwezerani ku dziko la Israeli. 13 Ndipo inu, anthu anga, mudzadziwa
kuti Ine ndine Yehova, pamene ndidzafukula manda anu ndikukutulut-
sanimo. 14 Ine ndidzayika Mzimu wanga mwa inu ndipo mudzakhalanso
ndi moyo. Pambuyo pake ndidzakulowetsani m'dziko lanulanu. Choncho
mudzadziwa kuti Ambuye Yehova ndayankhula zimenezi, ndipo ndidzazi-
chitadi. Ndikutero Ine Yehova!' "

### *Dziko Limodzi Kutsogoleredwa ndi Mfumu Imodzi*

15 Yehova anandiyankhula kuti: 16 "Iwe mwana wa munthu, tenga
ndodo ndipo ulembepo kuti, 'Ndodo ya Yuda ndi Aisraeli oyanjana nawo.'
Utengenso ndodo ina ndipo ulembepo kuti, 'Ndodo ya Efereimu, ndiye
kuti fuko la Yosefe ndi Aisraeli onse oyanjana nawo.' 17 Ulumikize ndodo
ziwirizi kuti zikhale ndodo imodzi m'dzanja lako.
18 "Anthu a mtundu wako akadzakufunsa tanthauzo la zimenezi
19 iwe udzawawuze mawu awa a Ine Ambuye Yehova akuti, 'Ine
ndidzatenga ndodo ya Yosefe imene ili m'dzanja la Efereimu, ndi ya
mafuko a Aisraeli oyanjana naye, ndi kuyilumikiza ku ndodo ya Yuda,
kuti zikhale ndodo imodzi, ndipo zidzakhaladi ndodo imodzi m'dzanja
langa!' 20 Ndodo ziwiri zimene udzalembepozo zikadzakhala m'manja
mwako pamaso pa anthu onse, 21 udzawawuze kuti Ine Ambuye Yehova
ndikuti: Ndidzawachotsa Aisraeli pakati pa anthu a mitundu ina kumene
anapita ku ukapolo. Ndidzawasonkhanitsa kuchokera ku mbali zonse ndi
kubwera nawo ku dziko lawolawo. 22 Ndidzawasandutsa mtundu umodzi
m'dzikomo, pa mapiri a Israeli. Padzakhala mfumu imodzi yowalamulira,
ndipo sadzakhalanso mitundu iwiri kapena kugawikana maufumu awiri.
23 Sadzadziyipitsanso ndi mafano awo, kapena ndi zinthu zawo zonyansa,
kapenanso ndi ntchito zawo zoyipa zilizonse. Ndidzawapulumutsa ku
machimo awo onse ndi kuwayeretsa. Choncho adzakhala anthu anga,
ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wawo.
24 " 'Mtumiki wanga Davide adzakhala mfumu yawo, motero onsewa
adzakhala ndi m'busa mmodzi. Iwo adzatsatira malamulo anga ndipo
adzasamalira kusunga malangizo anga. 25 Iwo adzakhala m'dziko limene
ndinalipereka kwa mtumiki wanga Yakobo, dziko limene makolo anu
ankakhalamo. Iwo ndi ana awo pamodzi ndi zidzukulu zawo adza-
khala kumeneko ndipo Davide adzakhala mfumu yawo kwa muyaya.

26 Ndidzachita nawo pangano lamtendere; lidzakhala pangano lamuyaya.
Ndidzawakhazikitsa ndi kuwachulukitsa, ndipo ndidzayika malo anga
opatulika pakati pawo kwamuyaya. 27 Nyumba yanga yokhalamo idza-
khala pakati pawo; Ine ndidzakhala Mulungu wawo, ndipo iwo adzakhala
anthu anga. 28 Pamenepo anthu a mitundu ina adzadziwa kuti Ine Yehova
ndiye amene ndimasandutsa Israeli kukhala woyera, pamene malo anga
opatulika adzakhala pakati pawo kwamuyaya!' "

# 38

*Za Chilango cha Gogi*

1 Yehova anandiyankhula kuti: 2 "Iwe mwana wa munthu, tembenukira
kwa Gogi, wa ku dziko la Magogi, amene ali kalonga wamkulu wa mzinda
wa Mesaki ndi Tubala. Umuyimbe mlandu. 3 Umuwuze mawu a Ine
Ambuye Yehova akuti, 'Ine ndikudana nawe, iwe Gogi, kalonga wamkulu
wa ku Mesaki ndi Tubala. 4 Ndidzakuzunguza, ndidzakukola ndi mbedza
m'kamwa mwako. Ndidzakutulutsa iweyo pamodzi ndi gulu lako lonse
la nkhondo, akavalo ako ndi okwerapo ake. Onse adzakhala atanyamula
zida za nkhondo, zishango ndi malihawo ndipo malupanga awo adzakhala
osolola. 5 Pamodzi ndi iwowo, padzakhalanso ankhondo a ku Perisiya, ku
Kusi, ndi ku Puti. Onsewa adzakhala atanyamula zishango ndi kuvala
zipewa zankhondo. 6 Padzakhalanso Gomeri pamodzi ndi ankhondo ake
onse ndiponso banja la Togarima ndi gulu lake lonse lankhondo lochokera
kutali kumpoto. Padzakhaladi mitundu yambiri ya anthu pamodzi ndi
iwe.

7 " 'Konzekani! Mukhaledi okonzeka, iweyo pamodzi ndi gulu lonse
la nkhondo limene lakusonkhanira. Iweyo udzawatsogolera pokamenya
nkhondo. 8 Pakapita masiku ambiri ndidzakuyitana. Zaka zikubwerazi
ndidzakulowetsa m'dziko limene lapulumuka ku nkhondo. Anthu ake ana-
sonkhanitsidwa kuchokera ku mitundu ya anthu ambiri n'kukakhazikika
pa mapiri a Israeli amene kwa nthawi yayitali anali ngati chipululu.
Anthu onsewa tsopano akukhala mwa mtendere. 9 Tsono iwe pamodzi ndi
ankhondo ako onse ndiponso mitundu yambiri ya anthu imene ili nawe
mudzabwera ngati mphepo yamkuntho. Mudzaphimba dziko lonse ngati
mitambo.

10 "Ine Ambuye Yehova ndikuti: Pa tsiku limenelo mu mtima mwako
mudzabwera maganizo ofuna kukonzekera kuchita zoyipa. 11 Iwe
udzanena kuti, 'Ndikukathira nkhondo dziko la midzi yopanda mi-
panda; ndikathira nkhondo anthu okhala mwamtendere, anthu amene
satchinjirizidwa ndi mipanda, zipata kapena mipiringidzo. 12 Ndipita
kukalanda chuma chawo ndi kukafunkha zinthu zawo. Ndidzalimbana
ndi midzi imene kale inali mabwinja. Ndikathira nkhondo anthu amene
anasonkhanitsidwa kuchokera kwa anthu a mitundu ina. Iwowa ali ndi
ziweto zambiri, katundu wochuluka ndiponso amakhala pakatikati pa
dziko lapansi.' 13 Anthu a ku Seba, a ku Dedani ndiponso amalonda a ku
Tarisisi pamodzi ndi midzi yake yonse adzakufunsa kuti, 'Kodi wabwera
kudzafunkha? Kodi wasonkhanitsa gulu lako la nkhondo kudzalanda
chuma, kudzatenga siliva ndi golide, ziweto ndi katundu kuti zikhale
zofunkha zochuluka?' "

14 "N'chifukwa chake, iwe mwana wa munthu, nenera ndipo uwuze
Gogi kuti, 'Ine Ambuye Yehova ndikuti: Pa nthawi imene anthu anga
adzakhala pa mtendere, iwe udzanyamuka. 15 Udzabwera kuchokera
ku dziko lako kutali kumpoto, iwe pamodzi ndi mitundu yambiri ya

anthu imene ili nawe, onse okwera akavalo, gulu lankhondo lalikulu ndi
lamphamvu. 16 Udzabwera kudzalimbana ndi anthu anga Aisraeli ngati
mtambo wophimba dziko. Masiku amenewo, iwe Gogi, ndidzabwera nawe
kuti ulimbane ndi dziko langa, kuti anthu a mitundu ina andidziwe Ine,
pamene ndidzaonetsa kuyera kwanga pa zimene ndidzakuchite iweyo.
17 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti: Kodi iwe si amene ndinayankhula za
iwe masiku amakedzana kudzera mwa atumiki anga aneneri a Israeli? Pa
zaka zambiri iwo ankalengeza kuti ndidzawutsa iwe kuti udzalimbane ndi
Israeli. 18 Zimene chidzachitika pa tsiku limenelo ndi izi: Gogi akadzathira
nkhondo dziko la Israeli, mkwiyo wanga woopsa udzayaka. Ndikutero
Ine Ambuye Wamphamvuzonse. 19 Chifukwa cha mkwiyo ndi ukali
wanga woyakawo Ine ndikunenetsa kuti pa nthawi imeneyo padzakhala
chivomerezi chachikulu m'dziko la Israeli. 20 Nsomba za m'nyanja,
mbalame zamumlengalenga, zirombo zakuthengo, cholengedwa chili-
chonse chimene chimakwawa pansi, ndiponso anthu onse okhala pa dziko
lapansi, adzanjenjemera pamaso panga. Mapiri adzang'ambika, malo
okwera kwambiri adzagumuka ndipo khoma lililonse lidzagwa pansi.
21 Ndidzawutsira Gogi nkhondo kuchokera ku mapiri anga. Ndikutero Ine
Ambuye Yehova. Anthu a Gogiyo adzaphana okhaokha ndi malupanga.
22 Ine ndidzamulanga ndi mliri ndi imfa. Ndidzagwetsa mvula yoopsa
ya matalala, ndiponso sulufule ndi miyala ya moto pa iye ndi pa
asilikali ake ndiponso pa mitundu yambiri ya anthu imene ili naye.
23 Motero ndidzadzionetsa kuti ndine wamphamvu ndi woyera. Ndiponso
ndidzadziwika pamaso pa anthu a mitundu ina yambiri. Momwemo
adzadziwadi kuti Ine ndine Yehova.' "

# 39

1 "Iwe mwana wa munthu, nenera modzudzula Gogi ndi kumuwuza
kuti Ine Ambuye Yehova ndikuti: 'Ine ndikudana nawe, iwe Gogi,
kalonga wamkulu wa Mesaki ndi Tubala. 2 Ine ndidzakuzunguza ndi
kukupirikitsira kutsogolo. Ndidzakutenga kuchokera kutali kumpoto ndi
kukutumiza kuti ukalimbane ndi anthu a ku mapiri a Israeli. 3 Kenaka Ine
ndidzathyola uta wa m'dzanja lako lamanzere ndipo ndidzagwetsa mivi ya
m'dzanja lako lamanja. 4 Udzagwa ku mapiri a ku Israeli, iwe ndi magulu
ako onse ankhondo ndiponso mitundu ya anthu imene ili nawe. Ndidza-
kusandutsa chakudya cha mitundu yonse ya mbalame zodya nyama,
ndiponso cha zirombo zakuthengo. 5 Udzafera pa mtetete kuthengo, pakuti
Ine ndayankhula. Ndikutero Ine Ambuye Yehova. 6 Ndidzatumiza moto pa
Magogi ndi pa onse amene amakhala mwamtendere m'mbali mwa nyanja.
Choncho adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.'
7 "Ndidzachititsa kuti dzina langa loyera lidziwike pakati pa anthu anga
Israeli. Sindidzalola kuti dzina langa liyipitsidwenso, ndipo mitundu ya
anthu idzadziwa kuti Ine Yehova ndine Woyera mu Israeli. 8 Zikubwera!
Ndipo zidzachitikadi, ndikutero Ine Ambuye Yehova. Ndiye tsiku limene
ndinanena lija.
9 "Pamenepo okhala m'mizinda ya Israeli adzatuluka ndipo adza-
sonkhanitsa zida zankhondo kuti zikhale nkhuni ndipo adzazitentha;
zishango ndi lihawo, mauta ndi mivi, zibonga za nkhondo ndi mikondo.
Adzazisonkhera moto kwa zaka zisanu ndi ziwiri. 10 Iwo sadzatolera
nkhuni kuthengo kapena kukadula ku nkhalango, chifukwa adzasonkhera
moto zidazo. Ndipo iwo adzafunkha amene anawafunkhawo, ndi kulanda
chuma cha amene anawalanda, ndikutero Ine Ambuye Yehova.

[11] “Pa tsiku limenelo ndidzamupatsa Gogi manda mu Israeli, m’chigwa
cha apaulendo, kummawa kwa Nyanja Yakufa. Mandawo adzatseka
njira ya apaulendo, chifukwa Gogi ndi gulu lake lankhondo adzayikidwa
kumeneko. Ndipo chigwacho chidzatchedwa chigwa cha gulu lankhondo
la Gogi.

[12] “Nyumba ya Israeli idzakhala ikukwirira mitembo kwa miyezi isanu
ndi iwiri ndi cholinga choyeretsa dziko. [13] Anthu onse a m’dzikomo
adzakwirira nawo mitembo. Ntchito imeneyo adzatchuka nayo pa tsiku
limene ndidzaonetsa ulemerero wanga. Ndikutero Ine Ambuye Yehova.

[14] “Patapita miyezi isanu ndi iwiri adzalemba ntchito anthu ena
odzayenda m’dziko lonse kufunafuna mitembo imene inatsalira
n’kumayikwirira. Choncho adzayeretseratu dzikolo. [15] Poyenda
m’dzikomo azidzati akaona fupa la munthu azidzayikapo chizindikiro
pambali pake mpaka okumba manda atakalikwirira fupalo ku chigwa cha
gulu lankhondo la Gogi. [16] (Komwekonso kudzakhala mzinda wotchedwa
Gulu la nkhondo). Ndipo potero adzayeretsa dziko.

[17] “Tsono iwe mwana wa munthu, Ine Ambuye Yehova ndikuti:
Itana mbalame za mitundu yonse ndi zirombo zonse zakuthengo ndipo
uziwuze kuti, ‘Sonkhanani ndipo bwerani kuchokera ku mbali zonse
ku nsembe imene ndikukonzerani inu, nsembe yayikulu pa mapiri a
Israeli. Kumeneko inu mudzadya mnofu ndi kumwa magazi. [18] Mudzadya
mnofu wa anthu ankhondo amphamvu ndi kumwa magazi a akalonga a
dziko lapansi. Onsewo anaphedwa ngati nkhosa zazimuna, ana ankhosa
onenepa, mbuzi ndiponso ngati ng’ombe zazimuna zonenepa za ku
Basani. [19] Ku phwando lansembe limene ndikukonzera inulo, mudzadya
zonona mpaka kukhuta ndi kumwa magazi mpaka kuledzera. [20] Pa tebulo
langa mudzakhuta pakudya akavalo ndi okwerapo ake, anthu amphamvu
ndi asilikali amitundumitundu,’ ndikutero Ine Ambuye Yehova.

[21] “Ine ndidzaonetsa ulemerero wanga pakati pa anthu a mitundu ina,
ndipo adzaona mmene ndidzawalangire ndikadzayika dzanja langa pa
iwo. [22] Kuyambira tsiku limenelo mpaka m’tsogolo Aisraeli adzadziwa
kuti Ine ndine Yehova Mulungu wawo. [23] Ndipo anthu a mitundu ina
adzadziwa kuti anthu a Israeli anatengedwa ukapolo chifukwa cha tchimo
lawo, chifukwa anali osakhulupirika kwa Ine. Choncho Ine ndinawabisira
nkhope yanga ndi kuwapereka kwa adani awo. Motero anaphedwa pa
nkhondo. [24] Ndinawachita zimenezi chifukwa cha kunyansa kwawo ndi
zolakwa zawo, ndipo ndinawabisira nkhope yanga.

[25] “N’chifukwa chake Ine Ambuye Yehova ndikuti: Tsopano ndidza-
khazikanso pa bwino banja la Yakobo. Ndidzachitira chifundo Ais-
raeli onse, ndipo ndidzateteza dzina langa loyera. [26] Anthuwo
akadzakhala mwamtendere m’dziko lawo popanda wina wowaopseza,
pamenepo adzayiwala zamanyazi zawo zimene zinawachitikira chifukwa
chosandikhulupirira Ine. [27] Ndidzawabwezeranso kwawo kuchokera
pakati pa anthu a mitundu ina ndipo ndidzawasonkhanitsa kuchokera
ku mayiko a adani awo. Poteropo ndidzaonetsa pamaso pa anthu a
mitundu yambiri kuti ndine Woyera. [28] Pamenepo iwo adzadziwa kuti Ine
ndine Yehova Mulungu wawo, ngakhale kuti ndinawapereka ku ukapolo
pakati pa anthu a mitundu ina. Ine ndidzawasonkhanitsanso ku dziko
lawo osasiyako wina m’mbuyo. [29] Ine sindidzawabisiranso nkhope yanga,
pakuti ndidzathira Mzimu wanga pa Aisraeli. Ndikutero Ine Ambuye
Yehova.”

# 40

*Malo Atsopano a Nyumba ya Mulungu*

1 Kumayambiriro a chaka cha 25, cha ukapolo wathu, tsiku la khumi
lamwezi, patapita zaka khumi ndi zinayi mzinda wa Yerusalemu uta-
wonongedwa, pa tsiku lomwelo dzanja la Yehova linali pa ine ndipo Iye
anapita nane ku Yerusalemu. 2 M'masomphenyawo Yehova ananditenga
ndi kupita nane ku dziko la Israeli ndipo anandiyika pa phiri lalitali
kwambiri, moti ndinaona ngati mzinda. 3 Atandifikitsa kumeneko
ndinaona munthu wonyezimira ngati mkuwa. Iye anali atayima pa
chipata ndipo m'dzanja lake munali chingwe cha nsalu yabafuta ndi
ndodo yoyezera. 4 Munthuyo anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu,
penyetsetsa ndipo umvetse bwinobwino. Uyikepo mtima wako pa zonse
zimene ndikukuonetsa pakuti anakubweretsa kuno kuti uwone zimenezi.
Tsono ukawawuze Aisraeli zonse zimene uzione."

*Chipata Chakummawa*

5 Ine ndinaona khoma litazungulira mbali zonse za Nyumba ya Mulungu.
M'dzanja la munthuyo munali bango lopimira limene kutalika kwake
kunali kwa mamita atatu. Atayeza chipupacho anapeza kuti kuchindikira
kwake kunali mamita atatu, ndiponso kutalika kwake kunalinso mamita
atatu.

6 Anapita ku chipata chakummawa. Anakwera pa makwerero a nyum-
bayo, nayeza chiwundo choyamba cha chipatacho; kutalika kwake kunali
mamita atatu. 7 Kudutsa chiwundo choyambachi, panali zipinda za alonda
zisanu ndi chimodzi, zitatu kudzanja lamanja, zitatu kudzanja lamanzere.
Chilichonse chinali cha mamita atatu mulitali mwake, chimodzimodzinso
mulifupi mwake. Mipata ya pakati pa zipindazo inali ya mamita awiri ndi
theka. Ndipo chiwundo cha pa chipata pafupi ndi khonde lapachipata,
chinali mamita atatu.

8 Ndipo iye anayeza khonde la chipata ndipo chinali cha mamita atatu.
9 Anayeza khonde ndipo linali mamita anayi. Mphuthu zake zinali mita
imodzi kuchindikira kwake. Khonde lam'kati lapachipata linali kumapeto
kwenikweni pafupi ndi Nyumba ya Mulungu.

10 M'kati mwa chipata chakummawa munali zipinda za alonda zitatu
mbali iliyonse. Zitatu zonsezo zinali zofanana, ndipo khonde la pakati pa
zipindazo linali lofanana. 11 Kenaka anayeza chipata cholowera; mulifupi
mwake munali mamita asanu ndipo mulitali mwake munali mamita asanu
ndi limodzi ndi theka. 12 Kutsogolo kwa chipinda chilichonse cha alonda
kunali khoma lalifupi lotalika theka la mita, ndipo mbali iliyonse ya
zipinda za alondazo inali yotalika mamita atatu. 13 Ndipo anayeza kutalika
kwa mulifupi mwa chipata cholowera, kuchokera ku khoma lakumbuyo
la chipinda chimodzi mpaka ku khoma la chipinda china; kuchokera
ku chitseko mpaka ku chitseko china. Kutalika kwake kunali mamita
khumi ndi awiri ndi theka. 14 Anayezanso khonde lam'kati ndipo linali
la mamita makumi atatu. Ndipo mozungulira khondelo munali bwalo.
Muyesowu sukuphatikiza khonde loyang'anana ndi bwalo. 15 Kuchokera
pa chipata cholowera mpaka ku mapeto a khonde la chipata, kutalika
kwake kunali mamita 27. 16 Makoma a zipinda ndiponso makoma a pakati
pa zipindazo anali ndi mazenera. Khonde lam'kati linalinso ndi mazenera
m'kati mwake. Pa makoma onsewo anajambulapo zithunzi za kanjedza.

*Bwalo la Kunja*

17 Kenaka munthuyo anandilowetsa m'bwalo lakunja, ndipo ndinaona
zipinda zina ndi msewu wa miyala wozungulira bwalo lonse. Zipinda
zonse zinali makumi atatu ndipo zinkayang'ana msewuwo. 18 Utali wa
mulifupi mwa msewuwo unkayenda mamita 27 kufanana ndi utali wa
chipata cholowera. Uwu unali msewu wa m'munsi. 19 Tsono, anayeza
kutalika kwa bwalo kuyambira chipata cholowera choyamba mpaka
polowera pa chipata chakunja cha bwalo la m'kati. Kutalika kwake kunali
mamita makumi asanu.

### *Chipata Chakumpoto*

20 Kenaka munthuyo anayeza mulitali ndi mulifupi mwa chipata
chimene chimayang'ana kumpoto, chotulukira kunja. 21 Zipinda za alonda
zimene zinalipo zitatu mbali iliyonse, makoma ake ndi khonde zinali ndi
muyeso wofanana ndi wachipata choyamba chija. Kutalika kwake kunali
mamita 27 ndipo mulifupi mwake munali mamita 13. 22 Mipata yake,
khonde lake ndi zojambula za kanjedza zinali ndi miyeso yofanana ndi za
chipata chakummawa. Chipatacho chinali ndi makwerero asanu ndi awiri
ndipo kotsirizira kwa chipatacho kunali khonde. 23 Panalinso chipata
cholowera ku bwalo lam'kati chofanana ndi chakummawa chimene
chimayang'anana ndi chipata chakumpoto, chofanana ndi cha mbali ya
kummawa. Anachiyeza kuchokera ku chipata china mpaka ku chipata
china. Kutalika kwake kunali mamita makumi asanu.

### *Chipata Chakummwera*

24 Ndipo munthuyo anapita nane ku mbali yakummwera ndipo ndinaona chipata chakummwera. Iye anayeza mphuthu zake ndi khonde
ndipo zinali ndi miyeso yofanana ndi ya zina zija. 25 M'zipinda za chipata
cholowera chimenechi ndi m'khonde lake munali mipata yofanana ndi
ya m'zipinda zina. Mulitali mwake munali mamita 27, mulifupi mwake
munali mamita 13. 26 Chipatacho chinali ndi makwerero asanu ndi
awiri ndi khonde kotsirizira kwake. Chipindacho chinali ndi zojambula
za kanjedza ku mbali zonse za makoma. 27 Bwalo lam'kati linalinso
ndi chipata kummwera. Munthuyo analiyeza kuchokera ku chipata
chimenechi mpaka ku chipata chakunja. Kutalika kwake kunali mamita
makumi asanu.

### *Zipata Zolowera ku Bwalo la M'kati*

28 Ndipo munthu uja anandilowetsa m'bwalo lam'kati kudzera ku
chipata chakummwera. Anayeza chipatachi ndipo chinali chofanana ndi
zinzake zija. 29 Zipinda zake za alonda, makoma ake ndi khonde lake
zinali zofanana ndi zina zija. Chipata cholowera ndi khonde lake zinali ndi
mipata m'mbali zonse. Mulitali mwake munali mamita 27 ndipo mulifupi
munali mamita 13. 30 (Khonde lililonse la makonde atatu a zipata zolowera
bwalo lam'kati aja linali la mamita ozungulira m'bwalo lam'kati anali
mamita 13 mulitali mwake, mamita awiri ndi theka mulifupi mwake).
31 Khonde lake linayang'anana ndi bwalo lakunja. Pa mphuthu pake
anajambulapo zithunzi za kanjedza mbali zonse ziwiri, ndipo linali ndi
makwerero asanu ndi atatu.

32 Kenaka munthuyo anapita nane ku bwalo la m'kati mbali ya
kummawa, ndipo anayeza chipata cholowera; chinali chofanana ndi
zinzake zina zija. 33 Zipinda zake za alonda, makoma ake ndi khonde
lake zinali zofanana ndi zina zija. Chipata cholowera ndi khonde lake
chinali ndi mipata m'mbali zonse. Mulitali mwake munali mamita 27

ndipo mulifupi mwake munali mamita 13. 34 Khonde lake linayang'anana
ndi bwalo lakunja. Pa mphuthu pake anajambulapo zithunzi za kanjedza
mbali zonse ziwiri, ndipo linali ndi makwerero asanu ndi atatu.

35 Kenaka anapita nane ku chipata chakumpoto ndipo anachiyeza.
Chinali chofanana ndi zina zija. 36 Zipinda zake za alonda, makoma ake
ndiponso khonde lake zinali zofanana ndi zina zija, ndipo chinalinso ndi
mipata mbali zonse ziwiri. Mulitali mwake munali mamita 27 ndipo
mulifupi mwake munali mamita 13. 37 Khonde lake limayang'anana ndi
bwalo lakunja. Pa mphuthu zake anajambulapo zithunzi za kanjedza
mbali zonse ziwiri, ndipo linali ndi makwerero asanu ndi atatu.

### *Zipinda Zokonzeramo Nsembe*

38 Panali chipinda ndipo khomo lake linali pafupi ndi khonde la chipata
cholowera cham'kati. M'chipinda m'menemo ankatsukira nyama ya
nsembe yopsereza. 39 Pa khonde la chipatacho panali matebulo awiri,
lina kuno lina uko. Ankapherapo nsembe zopsereza, nsembe zopepesera
machimo ndi nsembe zopepesera kupalamula. 40 Panali matebulo anayi,
awiri a iwo anali kunja kwa khoma la khonde pafupi ndi makwerero
olowera pa chipata chakumpoto ndi awiri enawo anali mbali inayo ya
makwerero. 41 Choncho ku mbali imodzi ya chipata kunali matebulo
anayi, ndiponso ku mbali inayo kunali matebulo anayi. Onse pamodzi
anali matebulo asanu ndi atatu. Pa matebulopo ankapherapo nyama
za nsembe zopsereza. 42 Matebulo anayiwa anali a miyala yosema.
Lililonse mulitali mwake linali la masentimita 75, mulifupi mwake linali
la masentimita 75, ndipo msinkhu wake unali wa masentimita makumi
asanu. Pa matebulopo amayikapo zipangizo zophera nsembe zopsereza
ndi nsembe zina. 43 Choncho pa matebulopo ankayikapo nyama za
nsembe zopsereza. Mbedza zitatu zazitali ngati chikhatho amazikoleka
pa makoma pozungulira ponse.

### *Zipinda za Ansembe*

44 Munthu uja anapita nane m'kati mwa bwalo ndipo ndinaona zipinda
ziwiri. Chimodzi chinali pafupi ndi chipata chakumpoto kuyang'ana
kummwera ndi china chinali pafupi ndi chipata chakummwera
kuyang'ana kumpoto. 45 Munthuyo anandiwuza kuti, "Chipinda chimene
chikuyang'ana kummwera ndi cha ansembe amene amayang'anira
Nyumba ya Mulungu, 46 ndipo chipinda chimene chikuyang'ana kumpoto
ndi cha ansembe amene amayang'anira guwa lansembe. Amenewa ndiwo
ana a Zadoki, ndipo ndi okhawo mwa zidzukulu za Levi amene ayenera
kutumikira pamaso pa Yehova m'Nyumba ya Mulungu."

47 Kenaka munthuyo anayeza bwalo; linali lofanana mbali zonse
kutalika kwake, mulitali mwake munali mamita 53, ndipo mulifupi mwake
munali mamita 53. Ndipo guwa lansembe linali kutsogolo kwa Nyumba
ya Mulungu.

### *Nyumba ya Mulungu*

48 Munthuyo anapita nane pa khonde la Nyumba ya Mulunguyo.
Anayeza mphuthu za khondelo ndipo zinali mamita awiri ndi theka
mbali zonse. Mulifupi mwa chipatacho munali mamita asanu ndi awiri
ndipo mulifupi mwa makoma ake munali mamita awiri mbali zonse.
49 Mulitali mwa khonde munali mamita khumi, mulifupi mwake munali
mamita asanu ndi limodzi kuchokera kutsogolo mpaka kumbuyo. Panali
makwerero khumi, ndipo mbali zonse kunali nsanamira.

# 41

[1] Ndipo munthuyo anapita nane m’chipinda chopatulika cha Nyumba
ya Mulungu ndipo anayeza khonde lake; mulifupi mwa khondelo munali
mamita atatu mbali iliyonse kutalika kwake. [2] Mulifupi mwa khomo
munali motalika mamita asanu. Makoma a mbali zonse anali a mamita
awiri ndi theka mulifupi mwake. Anayezanso kutalika kwa chipinda
chopatulika chija ndipo mulitali mwake munali motalika mamita makumi
awiri ndi mulifupi mwake munali mamita khumi.

[3] Kenaka munthuyo anakalowa m’kati ndipo anayeza khonde la pa
khomo; khondelo linali mita imodzi mulifupi mwake. Mulifupi mwa
khondelo munali mamita atatu. [4] Ndiponso anayeza kutalika kwa chipinda
chopatulika chenichenicho. Mulitali mwake munali mamita khumi, ndipo
mulifupi mwake munali mamita khumi. Munthuyo anandiwuza kuti, “Ichi
ndicho chipinda chopatulika kwambiri.”

[5] Tsono munthuyo anayeza khoma la Nyumba ya Mulungu; kuchindikira
kwake kunali mamita atatu. Panalinso zipinda zina kuzungulira Nyumba
ya Mulungu ndipo chilichonse chinali cha mamita awiri mulifupi wake.
[6] Zipindazo zinali zitatu zosanjikizana. Chigawo chilichonse chinali ndi
zipinda makumi atatu. Pa makoma a Nyumba ya Mulungu panali zochirik-
iza zipindazo kuti zisatsamire khoma la Nyumba ya Mulungu. [7] Zipinda
za m’mbalizo zinkapita zikulirakulira pomakwera chipinda ndi chipinda
potsata kukulirakulira kwa zochirikiza za zipinda zija. Pambali pa
Nyumba ya Mulungu panali makwerero okwerera pamwamba, kuchokera
chigawo chapansi kudzera chapakati, mpaka kukafika pamwamba.

[8] Ndinaona chiwundo kuzungulira Nyumba ya Mulungu. Chinapanga
maziko a zipindazo ndipo chinali cha mamita atatu. [9] Khoma lakunja la
zipindazo linali la mamita awiri ndi theka kuchindikira kwake. Pakati
pa chiwundocho [10] ndi zipinda za Nyumba ya Mulungu panali bwalo
limeneli la mamita khumi kupingasa kwake kuzungulira Nyumba yonse
ya Mulungu. [11] Zitseko za zipinda zam’mbalizo zinali zotsekulira ku
chiwundo. Chitseko chimodzi chinkayang’ana kumpoto ndipo china
chinkayang’ana kummwera. Chiwundo chosamangapo kanthu chinali
mamita awiri ndi theka kukula kwake kuzungulira ponseponse.

[12] Nyumba imene inali chakummwera moyang’anana ndi bwalo la
Nyumba ya Mulungu inali mamita 35 mulifupi mwake. Khoma la
nyumbayo linali mamita awiri ndi theka kuchindikira kwake kuzungulira
ponseponse, ndipo mulitali mwake linali mamita 45.

[13] Ndipo munthuyo anayeza Nyumba ya Mulungu ndipo mulitali mwake
inali mamita makumi asanu. Nyumbayo ndi makoma ake, zonse zinali
za mamita makumi asanu. [14] Kumaso kwa Nyumba ya Mulungu
chakummawa kwa bwalolo mulifupi mwake munali mamita makumi
asanu.

[15] Kenaka anayeza kutalika kwa nyumba yoyang’anana ndi bwalo
chakumadzulo kwa Nyumba ya Mulungu, kuphatikizapo njira zam’kati
ku mbali iliyonse. Kutalika kwake kunali mamita makumi asanu.

Chipinda chachikulu cha Nyumba ya Mulungu, chimene chili cham’kati,
khonde lam’kati loyang’anana ndi bwalo, [16] mazenera ndi maferemu
ake, zonsezi zinali zokutidwa ndi matabwa. Pamwamba moyang’anana
ndi chiwundo, Nyumba ya Mulungu inakutidwa ndi matabwa kuyambira
pansi mpaka ku mazenera, (mazenerawo anali okutidwa), [17] pamwamba
pa khomo lolowera ku malo opatulika am’kati komanso kuzungulira

makoma onse kunja ndi m'kati, 18 anajambulapo zithunzi za kerubi
mmodzi atakhala pakati pa kanjedza muwiri. Kerubi aliyense anali ndi
nkhope ziwiri: 19 imodzi inali nkhope ya munthu yoyang'ana kanjedza
mbali imodzi, ndi ina inali nkhope ya mkango yoyang'ana kanjedza mbali
ina. Zinajambulidwa kuzungulira Nyumba ya Mulungu yonse. 20 Motero
kuyambira pansi mpaka pamwamba pa khomo komanso pa makoma onse
a chipinda chachikulu cha Nyumba ya Mulungu, anajambula zithunzi za
akerubi ndi kanjedza pa makoma onse a malo opatulika.
21 Mphuthu za chipinda chachikulu cha Nyumba ya Mulungu kutalika
kwake mbali zonse kunali kofanana. Ndipo kumaso kwa malo opatulika
kunali chinthu china chooneka ngati 22 guwa lansembe la matabwa.
Msinkhu wake unali mita imodzi ndi theka, mulitali mwake munali
mita imodzi, mulifupi mwake munalinso mita imodzi. Mphuthu zake,
tsinde lake ndi mbali zonse zinali za matabwa. Munthuyo anandiwuza
kuti, "Tebulo limeneli ndilo limakhala pamaso pa Yehova." 23 Chipinda
chachikulu chija chinali ndi zitseko ziwiri. Malo opatulika aja analinso
ndi zitseko ziwiri. 24 Chitseko chilichonse chinali ndi zigawo ziwiri
zopatukana. 25 Ndipo pa zitsekopo anajambulipo zithunzi za akerubi ndi
kanjedza monga zomwe anajambulapo pa makoma. Kunja kwake kunali
ngati denga lamatabwa pamwamba pa khonde lam'kati. 26 Pa mbali
zonse za khonde lam'katilo panali mazenera, ndipo pa makoma ake onse
anajambulapo zithunzi za kanjedza.

# 42

*Zipinda za Ansembe*

1 Pambuyo pake munthuyo anapita nane ku bwalo lakunja chakumpoto
ndipo anafika nane ku zipinda zoyang'anana ndi bwalo la Nyumba
ya Mulungu ndi nyumba ina yakumpoto. 2 Nyumba yakumpotoyi
mulitali mwake munali mamita makumi asanu, mulifupi mwake munali
mamita 25. 3 Panali midadada iwiri, umodzi umayang'anana ndi
bwalo lam'kati la mamita khumi, winawo umayang'anana ndi bwalo
lakunja. Midadada iwiriyi inali ya nyumba zitatu zosanjikana ndipo
imayang'anana. 4 Kumaso kwa zipindazo kunali njira yam'kati, mulifupi
mwake munali mamita asanu, mulitali mwake munali mamita makumi
asanu. Makomo ake analoza chakumpoto. 5 Zipinda zammwamba
zinali zazifupi m'mimbamu kupambana zipinda zam'munsi ndi zipinda
zapakati chifukwa njira zake zinatenga malo ambiri. 6 Popeza zipinda
zinali zosanjikizana katatu ndipo zinalibe nsanamira monga za mabwalo,
motero zipinda zam'mwamba zinali zochepa kuyerekeza ndi zipinda
zapansi ndi zipinda zapakati. 7 Panali khoma lakunja lomwe limatsatana
ndi zipindazo kutsogolo kwake pambali pabwalo lakunja, kutalika kwake
kunali mamita 25. 8 Zipinda za m'mbali mwa bwalo lakunja mulitali
mwake munali mamita 25. Koma zomwe zinali m'mbali mwa Nyumba
ya Mulungu, mulitali mwake munali mamita makumi asanu. 9 Pansi
pa zipinda zimenezi panali khomo chakummawa kuchokera ku bwalo
lakunja kumene khoma lake linkayambira.
10 Mbali yakummwera kuyang'anana ndi bwalo ndi nyumbayo kunali
zipinda zina. 11 Kumaso kwa zipindazi kunali njira. Zipindazi mulitali
mwake, mulifupi mwake ndiponso maonekedwe ake onse zinali zofanana
ndi zipinda zoyang'ana zakumpoto zija. Makomo ndi zitseko zake
zinalinso zofanana 12 ndi makomo a zipinda zakummwera. Kunali khomo

m'mbali ya kummawa kumene ankalowerako. Kunalinso khoma logawa
zipinda.
[13] Ndipo munthuyo anandiwuza kuti, "Zipinda zakumpoto ndi za-
kummwera zoyang'anana ndi bwalo la Nyumba ya Mulungu ndi zoyera.
M'menemo ansembe amene amakhala pafupi ndi Yehova amadyeramo
zopereka zopatulika kwambiri. M'menemo adzayikamo zopereka zopat-
ulika kwambiri, zopereka za chakudya, nsembe zopepesera machimo ndi
nsembe zopepesera kupalamula, poti malowo ndi opatulika. [14] Pamene
ansembe alowa ku malo opatulikawa, asatuluke kupita ku bwalo lakunja
popanda kusiya momwemo zovala zimene anavala potumikira zija, pakuti
zovalazi ndi zopatulika. Avale kaye zovala zina ndipo akhoza kufika kwa
anthu."
[15] Munthuyo atamaliza kuyeza zimene zinali m'kati mwa Nyumba ya
Mulungu, anatuluka nane pa chipata chakummawa ndi kuyeza bwalo
lonse. [16] Anayeza mbali yakummawa ndi ndodo yake yoyezera; kutalika
kwake kunali mamita 250. [17] Anayeza mbali ya kumpoto ndi ndodo
yake; kutalika kwake kunali mamita 250. [18] Munthuyo anayeza mbali
yakummwera; kutalika kwake kunali mamita 250 atayeza ndi ndodo
yake. [19] Kenaka anatembenukira ku mbali ya kumadzulo ndi kuyeza ndi
ndodo yake; kutalika kwake kunali mamita 250 atayeza ndi ndodo yake.
[20] Motero anayeza mbali zonse zinayi. Panali khoma lozungulira bwalolo
mulitali mwake munali mamita 250 ndipo mulifupi mwake munalinso
mamita 250. Khomalo linali lolekanitsa zinthu zoyera ndi zinthu wamba.

# 43

*Ulemerero Ubwerera M'nyumba ya Mulungu*

[1] Pambuyo pake munthuyo anapita nane ku chipinda choyang'ana
kummawa, [2] ndipo ndinaona ulemerero wa Mulungu wa Israeli ukub-
wera kuchokera kummawa. Liwu lake linali ngati mkokomo wamadzi,
ndipo dziko linawala ndi ulemerero wake. [3] Masomphenya amene
ndinawaonawa anali ngati masomphenya amene ndinawaona pamene
Yehova anabwera kudzawononga mzinda ndiponso ngati masomphenya
amene ndinawaona ku mtsinje wa Kebara. Ndipo ndinadzigwetsa chafufu-
mimba. [4] Ulemerero wa Yehova unalowa m'Nyumba ya Mulungu kudzera
pa chipata choyang'ana kummawa. [5] Tsono Mzimu unandinyamula
nundilowetsa m'bwalo lam'kati, ndipo ulemerero wa Yehova unadzaza
Nyumba ya Mulungu.
[6] Munthuyo ali chiyimire pambali panga, ndinamva wina
akundiyankhula kuchokera m'Nyumba ya Mulungu. [7] Iye anandiwuza
kuti, "Iwe mwana wa munthu, awa ndi malo a mpando wanga waufumu,
ndi malo opondapo mapazi anga. Pano ndiye pamene ndidzakhala pakati
pa Aisraeli mpaka muyaya. Aisraeliwa kapena mafumu awo sadzayipitsa
dzina langa popembedza milungu ina kapena poyika mitembo ya mafumu
awo ku zitunda zachipembedzo. [8] Ankamanga chiwundo chawo pafupi
ndi chiwundo changa, ndiponso mphuthu zawo pafupi ndi mphuthu
zanga, n'kungokhala khoma chabe pakati pa iwowo ndi Ine. Motero
anayipitsa dzina langa loyera ndi machitidwe awo onyansa. Choncho
Ine ndinawawononga ndili wokwiya. [9] Tsopano alekeretu kupembedza
milungu ina ndipo achotseretu mitembo ya mafumu awo, isakhale pafupi
ndi Ine, ndipo Ine ndidzakhala pakati pawo mpaka muyaya.

10 "Iwe mwana wa munthu, awuze Aisraeliwa za Nyumba ya Mulunguyi,
mamangidwe ake ndipo achite manyazi ndi machimo awo, 11 akachita
manyazi ndi zoyipa zonse anachita, uwafotokozera za Nyumba ya
Mulungu, mamangidwe ake, makomo ake otulukira ndi makomo olowera,
ndiye kuti, mamangidwe ake onse. Uwafotokozerenso malangizo ndi
malamulo ake. Uwalembe akuona kuti athe kuwasunga ndi kuwachita.
12 "Limeneli ndi lamulo la Nyumba ya Mulungu imene idzamangidwe
pamwamba pa phiri. Malo ake onse ozungulira adzakhala oyera
kwambiri. Limeneli ndilo lamulo la Nyumba ya Mulungu.

### *Guwa la Nsembe*

13 "Miyeso ya guwa lansembe ndi iyi: Pa tsinde pake padzakhala
ngalande ya masentimita makumi asanu kuzama kwake ndi mulifupi
mwake. M'phepete mwa ngalandeyo kuzungulira guwa lonse, mudza-
khala mkombero wa masentimita 25. 14 Kuchokera m'ngalande ya pansi
padzakhala mpaka pa phaka lapansi mita imodzi, mulifupi mwake theka
la mita. Kuchokera pa phaka laling'ono mpaka pa phaka lalikulu, msinkhu
wake ndi mamita awiri, mulifupi mwake ndi masentimita makumi asanu.
15 Malo osonkhapo moto pa guwa, msinkhu wake udzakhala mamita
awiri. Pa ngodya iliyonse ya malo osonkhapo motowo panatuluka nyanga
imodzi. 16 Malo osankhalapo moto pa guwa lansembe miyeso yake ndi
yofanana mbali zonse. Mulitali mwake mudzakhala mamita asanu ndi
limodzi ndipo mulifupi mwake mudzakhalanso mamita asanu ndi limodzi.
17 Phaka lapamwamba muyeso wake udzakhala wofanana mbali zonse.
Mulitali mudzakhala mamita asanu ndi awiri ndiponso mulifupi mwake
mudzakhalanso mamita asanu ndi awiri. Mkombero wake udzakhala
wa masentimita 25 ndiponso ngalande yake yozungulira idzakhala ya
masentimita 25. Makwerero a guwa lansembe adzayang'ana kummawa."
18 Kenaka munthuyo anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu,
Ambuye Yehova akuti: Guwalo litamangidwa, tsono malamulo awa
azidzatsatidwa popereka nsembe zopsereza ndiponso powaza magazi pa
guwapo. 19 Udzawapatse ansembe, omwe ndi Alevi, a banja la Zadoki,
amene amabwera pafupi nane kudzanditumikira, mwana wang'ombe
wamwamuna kuti aperekere nsembe yopepesera machimo. Ndikutero
Ine Ambuye Yehova. 20 Udzatengeko magazi ake ena ndi kuwapaka pa
nyanga zinayi za pa guwa lansembe, pa ngodya zinayi za phaka ndiponso
mozungulira mkombero wonse. Motero udzaliyeretsa ndi kulipatula.
21 Udzatenge ng'ombe yayimuna yomwe yaperekedwa ngati nsembe
yopepesera machimo, ndipo udzayiwotche pa malo ake enieni m'bwalo
la Nyumba ya Mulungu, kunja kwa malo opatulika.
22 "Mmawa mwake udzatenge mbuzi yopanda chilema kuti nayonso
iperekedwe ngati nsembe yopepesera machimo. Pambuyo pake idza-
yeretse guwa lansembe monga unachitira ndi ng'ombe yayimuna ija.
23 Utatha kuyeretsa guwa lansembelo, udzatenge mwana wang'ombe
wamwamuna wopanda chilema ndiponso nkhosa yayimuna yopanda
chilema. 24 Udzapereke zonsezi pamaso pa Yehova, ndipo ansembe
adzazithire mchere ndi kuzipereka kuti zikhale nsembe zopsereza kwa
Yehova.
25 "Kwa masiku asanu ndi awiri, uzidzapereka tsiku ndi tsiku mbuzi
yayimuna, mwana wang'ombe, ndiponso nkhosa kuti zikhale nsembe
zopepesera machimo. Zonsezi zidzakhale zopanda chilema. 26 Kwa
masiku asanu ndi awiriwo ansembe adzachite mwambo woyeretsa ndi

kupatula guwa lansembelo. 27 Masiku amenewa atatha, kuyambira
tsiku lachisanu ndi chitatu, ansembe azipereka nsembe zanu zopsereza
ndi nsembe zachiyanjano pa guwa lansembe. Apo ndidzakulandirani.
Ndikutero Ine Ambuye Yehova."

# 44

*Mfumu, Alevi ndi Ansembe*

1 Munthu uja anabwerera nane ku chipata chakunja kwa malo opat-
ulika, chomwe chimayang'ana kummawa. Chipatacho chinali chotseka.
2 Yehova anandiwuza kuti, "Chipata ichi chikhale chotseka, chisat-
sekulidwe. Wina asalowerepo chifukwa Yehova, Mulungu wa Israeli
walowera pomwepa. 3 Kalonga yekha angathe kukhala m'menemo ndi
kumadya chakudya pamaso pa Yehova. Iye adzalowere pa njira ya ku
khonde lam'kati ndi kutulukiranso njira yomweyo."

4 Kenaka munthuyo anandidzeretsa pa chipata chakumpoto ndipo
tinafika kumaso kwa Nyumba ya Mulungu. Nditapenyetsetsa ndinan-
goona ulemerero wa Yehova utadzaza m'Nyumba ya Mulungu, ndipo
ndinadzigwetsa pansi chafufumimba.

5 Yehova anandiwuza kuti, "Iwe mwana wa munthu, samala bwino
ndipo uyang'anitsitse ndi kumvetsa bwino zonse zimene ndikuwuze
zokhudza malamulo ndi malangizo a Nyumbayi. Usamalitse za amene
angalowe ndi kutuluka m'Nyumbayi. 6 Uwuze mtundu wopanduka
wa Israeli kuti Ine Ambuye Yehova ndikuti: Inu Aisraeli, andikwana
machitidwe anu onyansawo! 7 Munalowetsa alendo osachita mdulidwe
mu mtima ndi m'thupi momwe m'Nyumba yanga ndipotu anayipitsa
Nyumba yanga. Pamene inu munkandipatsa chakudya changa ndi magazi
omwe kuwonjezera pa zonyansa zanu zonse ndiye kuti munaphwanya
pangano langa. 8 M'malo moti muzisamalira zinthu zanga zopatulika,
mwayika alendo kuti aziyang'anira malo anga opatulika. 9 Ambuye
Wamphamvuzonse akuti: Palibe mlendo wosachita mdulidwe mu mtima
ndi m'thupi ngakhalenso mlendo amene amakhala pakati pa Aisraeli
amene adzalowe m'malo anga opatulika.

10 "Ndiponso Alevi amene anandisiya kutali pa nthawi imene Israeli
anasochera potsata mafano, adzalangidwa chifukwa cha tchimo lawo.
11 Adzangokhala atumiki chabe m'malo anga opatulika. Azidzayang'anira
zipata za Nyumba ya Mulungu ndi kugwira ntchito kumeneko. Azidzapha
nyama za nsembe zopsereza ndi za nsembe zina za anthu. Choncho
azidzayimirira pamaso pa anthu n'kumawatumikira. 12 Iwowa anka-
tumikira anthu popembedza mafano awo, ndipo anachititsa Aisraeli
kugwa mu uchimo. N'chifukwa chake Ine ndikulumbira kuti iwowa
ayenera kulangidwa chifukwa cha machimo awo. Ndikutero Ine Ambuye
Yehova. 13 Iwo sayenera kufika pafupi ndi Ine ndi kunditumikira ngati
ansembe, kapena kuyandikira chilichonse cha zinthu zanga zopatulika,
kapenanso zopereka zanga zopatulika kwambiri. Iwo adzachititsidwa
manyazi chifukwa cha machitidwe awo onyansa. 14 Komabe ndidzawayika
kuti aziyang'anira Nyumba yanga ndi kutumikira pa ntchito zake zonse
zoyenera kuti zigwiridwe m'menemo.

15 "Koma ansembe, a fuko la Levi, a banja la Zadoki amene anka-
tumikira mokhulupirika ku malo anga opatulika pa nthawi imene
Aisraeli anasochera ndi kundisiya Ine; iwowa adzasendera kwa Ine
kudzanditumikira. Adzafika pamaso panga kuti apereke nsembe za

mafuta ndi magazi. Ndikutero Ine Ambuye Yehova. [16] Okhawa ndiwo
adzalowe ku malo anga opatulika ndi kudzayandikira tebulo langa kuti
adzanditumikire. Amenewa okha ndiwo adzasamalire zinthu zanga.
[17] "Pamene alowa ku zipata za bwalo lam'kati azivala zovala zabafuta.
Asamavale chovala china chilichonse cha ubweya wankhosa pamene
akutumikira pa zipata za bwalo la m'kati kapena kunja kwa Nyumba ya
Mulungu. [18] Azivala nduwira za bafuta ndi kabudula wabafuta m'kati.
Asavale chilichonse chowachititsa thukuta. [19] Pamene atuluka ndi kupita
ku bwalo lakunja kumene kuli anthu, azivula zovala zimene amatumikira
nazo, ndipo azisiye zovalazo mu zipinda zopatulika. Pambuyo pake avale
zovala zina, kuopa kuti angapatsireko kuyera anthu enawo ndi zovala
zawozo.
[20] " 'Ansembe asamamete mpala kapena kusunga tsitsi lalitali kwambiri,
koma azingoliyepula. [21] Wansembe asamwe vinyo pamene ali pafupi
kulowa m'bwalo la m'kati. [22] Iwo asakwatire akazi amasiye kapena
osudzulidwa; koma azikwatira anamwali osadziwa mwamuna a fuko la
Israeli kapena akazi amasiye a ansembe anzawo. [23] Ansembe aziphunzitsa
anthu anga kusiyanitsa pakati pa zinthu zopatulika ndi zinthu wamba,
ndiponso pakati pa zinthu zoyenera ndi zosayenera kuperekedwa nsembe.
[24] " 'Pakakhala milandu, ansembe azikhala oweruza ndipo agamule
milanduyo potsata malamulo anga. Atsate malamulo anga ndi malangizo
anga pa za masiku anga onse a chikondwerero. Asamalirenso kuti masiku
anga a Sabata akhale oyera.
[25] " 'Wansembe asadziyipitse pokhudza munthu wakufa, pokhapokha
ngati wakufayo ndi abambo ake kapena amayi ake, mwana wake wamwa-
muna kapena wamkazi, m'bale wake kapena mlongo wake wosakwatiwa.
[26] Atatha kuyeretsedwa adikirebe masiku asanu ndi awiri kuti ayere
ndithu. [27] Pa tsiku lomwe akukalowa m'bwalo la m'kati la malo opatulika
kuti akatumikire, apereke nsembe yopepesera machimo. Ndikutero Ine
Ambuye Yehova.
[28] " 'Ansembe asadzakhale ndi cholowa chilichonse ayi. Cholowa chawo
ndi Ine. Musadzawapatse chuma mu Israeli; Ine ndidzakhala chuma
chawo. [29] Iwo azidzadya nsembe ya chakudya, nsembe yopereka chifukwa
cha tchimo ndi nsembe yopepesera machimo. Zinthu zonse zoperekedwa
kwa Yehova mu Israeli zidzakhala zawo. [30] Zabwino za zipatso zanu
zoyambirira kucha ndiponso mphatso zanu zonse zapadera zidzakhala
za ansembe. Inu muziwapatsa chigawo choyamba cha ufa wanu kuti pa
nyumba panu pakhale madalitso. [31] Ansembe sayenera kudya kalikonse
kofa kokha, kaya mbalame, kapena nyama. Kapena yochita kujiwa.' "

# 45

*Magawidwe a Dziko*

[1] " 'Mukamadzagawa dziko kuti fuko lililonse lilandire cholowa chake,
mudzapatuleko chigawo chimodzi kuti chikhale cha Yehova. Mulitali
mwake mudzakhale makilomita khumi ndi awiri ndi theka ndipo mulifupi
mwake makilomita khumi. Malo onsewo adzakhale opatulika. [2] M'kati
mwa chigawo chimenechi, malo a mamita 250 mbali iliyonse adzakhala
malo a Nyumba ya Mulungu. Pozungulira pake ponse padzakhala malo
a mamita 25. [3] M'chigawo chopatulikacho muyeze malo a makilomita 12
ndi theka mulitali mwake, makilomita asanu mulifupi mwake. Pamenepo
padzakhala malo opatulika kwambiri. [4] Malo opatulika amenewa

adzakhalanso a ansembe amene amatumikira ku malo opatulika, amene
amayandikira Yehova kuti amutumikire. Pamenepo padzakhala malo
omangapo nyumba zawo ndi malo omangapo Nyumba ya Mulungu. 5 Alevi
otumikira ku Nyumba ya Mulungu adzakhala ndi malo a makilomita
khumi ndi awiri ndi theka mulitali mwake ndi makilomita asanu mulifupi
mwake. Kumeneko ndiko kudzakhale midzi yawo.

6 " 'Moyandikana ndi malo opatulika, padzakhale malo a makilomita
awiri ndi theka mulifupi mwake ndi makilomita khumi ndi awiri ndi theka
mulitali mwake; kuti akhale malo a mzinda. Malo amenewa adzakhala a
Aisraeli onse.
7 " 'Mfumu idzakhale ndi malo okhudzana ndi chigawo cha malo opat-
ulika ndi cha mzinda. Malowo ayandikane ndi zigawozo chakummawa
ndi chakumadzulo. Malowo atalike ngati chigawo chimodzi cha fuko la
Israeli kuyambira ku malire akummawa mpaka ku malire akumadzulo.
8 Malowa adzakhala chigawo cha mfumu mu Israeli. Choncho mafumu
anga sadzazunzanso anthu anga, koma adzidzalola Aisraeli kuti akhale
ndi zigawo zawozawo.

9 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti: Tsono pakwana, inu akalonga a Israeli.
Lekani nkhanza zanu ndi kupondereza anthu anga. Muzitsata chilungamo
ndi kuchita zokomera anthu. Musapirikitse anthu anga m'dzikomo.
Ndikutero Ine Ambuye Yehova. 10 Miyeso yanu yoyezera zinthu monga efa
ndi bati zizikhala zokhulupirika. 11 Efa ndi bati ikhale miyeso yolingana
kukula kwake. Muyeso wa homeri ukhale wokwanira mabati khumi,
ukhalenso wokwanira maefa khumi. Ndiye kuti kukula kwa miyeso
iwiriyo kuzidzatsata kukula kwa homeriyo. 12 Muyeso wa sekeli ukhale
wokwanira magera makumi awiri. Muyeso wa mina ukhale wolemera
masekeli 60.

### *Zopereka ndi Masiku Achikondwerero*

13 " 'Zopereka zomwe mudzidzapereka ndi izi: chimodzi mwa zigawo
60 za tirigu, barelenso chimodzimodzi ndiponso gawo limodzi la magawo
asanu ndi limodzi la efa, kulitapa pa barele wa homeri. 14 Gawo loyenera
la mafuta, loyezedwa ndi bati, ndiponso chigawo mwa zigawo 100 za
mafuta. Miyeso yake ili motere: mabati khumi afanana ndi homeri
imodzi kapena kori imodzi. 15 Muperekenso nkhosa imodzi pa gulu
lankhosa 200 za pa msipu wabwino wa mu Israeli. Izi zidzagwiritsidwa
ntchito monga nsembe za chakudya, nsembe zopsereza, ndi nsembe
zachiyanjano ndi nsembe zopepesera milandu ya anthu. Ndikutero Ine
Ambuye Yehova. 16 Anthu onse a m'dzikomo azidzapereka zimenezi kwa
mfumu ya Israeli. 17 Udzakhala udindo wa mfumu kupereka zofunikira
ku nsembe zopsereza, nsembe za chakudya, ndi nsembe za zakumwa pa
nthawi ya zikondwerero, chikondwerero cha mwezi watsopano ndi cha
masabata, nthawi yonse ya zikondwerero zoyikika za Aisraeli. Mfumuyo
idzapereka nsembe zopepesera machimo, nsembe za chakudya, nsembe
zopsereza, ndi nsembe zachiyanjano kuti zikhale nsembe zopepesera
machimo a Aisraeli.
18 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti: Pa tsiku loyamba la mwezi woyamba
muzitenga mwana wang'ombe wamwamuna wopanda chilema ndi ku-
chita mwambo woyeretsa malo opatulika. 19 Wansembe atengeko magazi
a nsembe yopepesera machimoyo ndipo awapake pa mphuthu za Nyumba
ya Mulungu, pa ngodya zinayi za pamwamba pa guwa lansembe ndi pa
mphuthu za pa chipata cha bwalo la m'kati. 20 Muzichita chimodzimodzi

pa tsiku la chisanu ndi chiwiri la mwezi, kuchitira aliyense amene
wachimwa mosafuna kapena mosadziwa. Motero Nyumba ya Mulungu
idzakhala yoyera.

21 " 'Pa tsiku la 14 la mwezi woyamba muzichita chikondwerero cha
Paska, chikondwerero chake cha masiku asanu ndi awiri. Pa masiku
amenewo muzidzadya buledi wopanda yisiti. 22 Pa tsiku loyamba
la chikondwererocho, mfumu ipereke nsembe ya ng'ombe yayimuna
monga nsembe yopepesera machimo ake ndi machimo a anthu onse a
m'dziko. 23 Pa masiku asanu ndi awiri a chikondwererocho, mfumu
ipereke kwa Yehova nsembe zopsereza izi: ng'ombe zazimuna zisanu ndi
ziwiri, nkhosa zazimuna zisanu ndi ziwiri, zonsezi zopanda chilema. Pa
masikuwa mfumu iziperekanso mbuzi imodzi yayimuna ngati nsembe
yopepesera machimo. 24 Pamodzi ndi ng'ombe iliyonse yayimuna ndi
nkhosa iliyonse yayimuna, mfumu ipereke chopereka cha chakudya
chokwanira efa imodzi ndiponso mafuta okwanira hini imodzi pa efa
iliyonse.

25 " 'Pa nthawi ya chikondwerero cha masiku asanu ndi awiri, chimene
chimayamba pa tsiku la 15 la mwezi wachisanu ndi chiwiri, mfu-
muyo iziperekanso nsembe za mtundu womwewo: nsembe zopepesera
machimo, nsembe zopsereza, nsembe za chakudya ndi za mafuta.' "

# 46

1 "Ambuye Yehova akuti, Chipata chakummawa cha bwalo lam'kati
chizikhala chotseka pa masiku asanu ndi limodzi ogwira ntchito, koma
chizitsekulidwa pa tsiku la sabata ndi pa tsiku la chikondwerero cha
mwezi watsopano. 2 Mfumu izilowa podzera m'khonde la m'kati la
chipata pochokera kunja, n'kudzayima pafupi ndi nsanamira yapakhomo.
Ansembe apereke nsembe yake yopsereza ndi nsembe yake yachiyanjano.
Mfumuyo ipembedze pa chiwundo cha pa chipatacho kenaka n'kutuluka.
Koma chipatacho asachitseke mpaka madzulo. 3 Anthu a m'dziko
azipembedza pamaso pa Yehova pa khomo la chipata chimenechi pa
masiku a sabata ndi pa tsiku la mwezi watsopano. 4 Nsembe yopsereza
imene mfumu iyenera kupereka kwa Yehova ikhale motere: pa tsiku
la Sabata izipereka ana ankhosa aamuna asanu ndi mmodzi wopanda
chilema, ndiponso nkhosa yayima yopanda chilema. 5 Pamodzi ndi nkhosa
yayimuna, mfumu izipereka nsembe ya chakudya yokwanira efa imodzi.
Pamodzi ndi ana ankhosa, mfumu izipereka monga ikufunira kutero.
Iperekenso hini imodzi ya mafuta pa efa iliyonse ya tirigu. 6 Pa tsiku la
mwezi watsopano mfumuyo ipereke mwana wang'ombe wamwamuna,
ana ankhosa asanu ndi mmodzi ndiponso nkhosa yayimuna, zonsezi
zopanda chilema. 7 Ipereke efa imodzi ya tirigu pa ng'ombe yayimuna
iliyonse ndiponso efa ina pa nkhosa yayimuna iliyonse. Pa ana ankhosa
ipereke tirigu monga ikufunira kutero. Pamodzi ndi efa ya tirigu, ipereke
hini imodzi ya mafuta. 8 Pamene mfumu ikulowa, izidzera m'khonde
lam'kati la chipata chakummawa, izitulukiranso pomwepo.

9 "Anthu a m'dzikomo akabwera kudzapembedza Yehova pa masiku
a chikondwerero, ngati munthu alowera pa chipata chakumpoto atu-
lukire chipata chakummwera. Munthu wolowera chipata chakummwera,
atulukire chipata chakumpoto. Munthu asatulukire pomwe walowera,
koma atulukire pa chipata choyang'anana nacho. 10 Mfumu izidzakhala

pakati pawo. Anthu akamadzalowa mfumu idzalowa nawo. Anthu
akamadzatuluka mfumu idzatuluka nawo.

11 "Pa masiku achikondwerero ndi pa masiku ena osankhidwa, zop-
ereka za chakudya zikhale zokwanira efa imodzi pamodzi ndi ng'ombe
yayimuna iliyonse, efa imodzinso ndi nkhosa yayimuna, koma pa mwana
wankhosa apereke monga angathere. Iperekenso hini imodzi ya mafuta
pa efa iliyonse. 12 Pamene mfumu ikufuna kupereka chopereka chaufulu
kwa Yehova, kaya ndi nsembe yopsereza kapena zopereka za chiyanjano,
ayitsekulire chipata chakummawa. Iyo ipereke nsembe yopsereza kapena
zopereka zake za chiyanjano monga imachitira pa tsiku la Sabata. Kenaka
ituluke ndipo mfumuyo itatuluka, atseke chitsekocho.

13 "Tsiku lililonse nthawi ya mmawa azipereka kwa Yehova mwana
wankhosa wa chaka chimodzi. 14 Pamodzi ndi nyamayo aziperekanso
mmawa uliwonse chopereka cha chakudya chokwanira chimodzi mwa
zigawo zisanu ndi chimodzi za efa. Aziperekanso chimodzi mwa zigawo
zitatu za hini ya mafuta okandira ufa wosalala. Chopereka cha chakudya
chimenechi chiziperekedwa kwa Yehova nthawi zonse mwa lamulo.
15 Motero azipereka mwana wankhosa ndi chopereka cha chakudya ndi
mafuta mmawa uliwonse kuti zikhale nsembe zopsereza za tsiku ndi tsiku.

16 " 'Ine Ambuye Yehova ndikuti: Ngati kalonga apereka mphatso
chigawo cha cholowa chake kwa mmodzi mwa ana ake, mphatsoyo
idzakhala ya ana akewo. Idzakhala yawo chifukwa ndi cholowa chawo.
17 Koma ngati ipereka mphatso yotere kuchokera pa cholowa chake kwa
mmodzi mwa antchito ake, mphatsoyo idzakhala ya wantchitoyo mpaka
chaka chaufulu. Pambuyo pake idzabwereranso kwa kalongayo chifukwa
cholowa chake ndi cha ana ake. 18 Kalonga asalande cholowa chilichonse
cha anthu, kuwachotsa m'dera lawo la dziko. Iye apereke kwa ana ake
cholowa chawo chochokera pa chuma chakechake, kuti pasapezeke ndi
mmodzi yemwe mwa anthu anga wolandidwa chuma chake.' "

19 Kenaka munthu uja anandidzeretsa pa khomo la pambali pa chipata
nandilowetsa ku zipinda za ansembe zoyang'ana kumpoto. Ndipo
ndinaona kumeneko malo chakumadzulo kwa zipindazo. 20 Munthuyo
anandiwuza kuti, "Awa ndi malo amene ansembe adzaphikirapo nsembe
yopepesera kupalamula ndi nsembe yopepesera machimo. Kumenekonso
azidzawotcherako chopereka cha chakudya. Sadzatuluka nazo zoyerazi
m'bwalo lakunja kuopa kuti angapatsireko kuyera anthu ena."

21 Pambuyo pake anandilowetsa m'bwalo lakunja napita nane ku
ngodya zinayi za bwalolo. Ndipo ndinaona m'kati mwa ngodya iliyonse
bwalo lina. 22 Motero pa ngodya zinayi za bwalo panalinso mabwalo
ena ang'onoang'ono. Mabwalo amenewa anali ofanana. Mulitali mwake
munali mamita makumi awiri ndipo mulifupi mwake munali mamita
khumi ndi asanu. 23 Kuzungulira mabwalo anayi ang'onoang'ono aja
panali mpanda wamiyala, ndi malo asonkhapo moto omangidwa m'munsi
mwa mpandawo mozungulira. 24 Munthuyo anandiwuza kuti, "Izi
ndi zipinda zophikiramo. M'menemu anthu otumikira ku Nyumba ya
Mulungu adzaphikiramo nyama za nsembe za anthu."

# 47

*Mtsinje Wotuluka M'nyumba ya Mulungu*

1 Munthuyo anabwerera nane ku chipata cha Nyumba ya Mulungu.
Ndinaona madzi akutuluka kunsi kwa chiwundo cha Nyumba ya Mu-
lungu chakummawa; poti Nyumba ya Mulungu inayang'ana kummawa.
Madziwo ankachokera kunsi kwa mbali yakummwera ya Nyumba ya
Mulungu; kummwera kwa guwa lansembe. 2 Ananditulutsira pa chipata
chakumpoto ndipo anazungulira nane panja mpaka ku chipata chakunja
choyang'ana kummawa. Ndipo ndinaona madzi akutuluka chakummwera
kwa chipatacho.

3 Munthuyo anapita chakummawa ali ndi chingwe choyezera m'dzanja
lake. Iye anayeza mamita 500, ndipo pambuyo pake analowa nane
m'madziwo amene ankalekeza m'kakolo. 4 Anayezanso mamita 500 ndipo
analowa nane m'madzi amene amalekeza m'mawondo. Iye anayezanso
mamita 500 ndipo analowa nane m'madzi amene amalekeza m'chiwuno.
5 Munthuyo anayezanso mamita 500, ndipo madziwo anasanduka mtsinje
woti sindikanatha kuwoloka, pakuti madziwo anakwera, ndipo anali
ozama ofunika kusambira pofuna kuwoloka. 6 Munthuyo anandifunsa
kuti: "Iwe mwana wa munthu, kodi ukuziona zimenezi?"

Kenaka anabwerera nane ku gombe la mtsinjewo. 7 Nditafika pa
gombepo, ndinaona mitengo yambiri ku mbali iliyonse ya mtsinjewo.
8 Tsono munthuyo anandiwuza kuti, "Madziwa akupita ku chigawo
chakummawa ndi kutsikira ku chigwa cha Araba. Kenaka akathira
m'Nyanja Yakufa, ndipo akakalowa m'nyanjayo, madzi a nyanjayo adza-
sanduka okoma. 9 Kulikonse kumene mtsinjewo ukuyenda cholengedwa
chilichonse chidzakhala ndi moyo. Nsombanso zidzakhala zambiri.
Paja madzi amenewa amapita kumeneko kuti akakometse madzi ena.
Choncho kulikonse kumene madziwa akuyenda chilichonse chidzakhala
ndi moyo. 10 Asodzi adzayima m'mbali mwa Nyanja Yakufa. Pakuti
kuchokera ku Eni-Gedi mpaka ku Eni Egilaimu kudzakhala malo oponyako
makoka. Kudzakhala nsomba zamitundumitundu, monga nsomba za ku
Nyanja Yayikulu. 11 Koma mathawale ake ndi maiwe ake sadzakhala
ndi madzi abwino; adzakhala ndi madzi a mchere. 12 M'mbali zonse
za mtsinje mudzamera mitengo ya zipatso zakudya za mtundu uliwonse.
Masamba ake sadzafota kapena kulephera kubereka zipatso. Izidzabereka
mwezi uliwonse, chifukwa madzi ake adzakhala ochokera ku Nyumba ya
Mulungu. Zipatso zake anthu azidzadya ndipo masamba ake azidzachitira
mankhwala."

### *Malire a Dziko*

13 Ambuye Yehova akuti, "Nawa malire amene mudzatsate powagawira
dziko mafuko khumi ndi awiri a Israeli aja. Yosefe adzalandire zigawo
ziwiri. 14 Mudzawagawire dzikolo mofanana. Paja ndinalumbira kwa
makolo anu kuti dzikoli lidzakhala lanulanu.

15 "Malire a dzikolo adzakhala motere:

Mbali ya kumpoto adzachokera ku Nyanja Yayikulu kutsata msewu wa
ku Hetiloni mpaka ku chipata cha Hamoti ndi kupitirira ku Zedadi,
16 Berota ndi Sibraimu (mizinda imene ili pakati pa malire a Damasiko
ndi Hamati mpaka kukafika ku Hazeri Hatikoni mzinda umene uli
m'malire mwa Haurani. 17 Motero malire akumpoto adzachokera
ku nyanja mpaka ku mzinda wa Hazari-Enoni, m'malire akumpoto
a Damasiko ndi chakumpoto kwa malire a Hamati. Awa adzakhala
malire a kumpoto.

18 Mbali ya kummawa malire adzayenda pakati pa Haurani ndi
Damasiko, mbali ya ku Yorodani pakati pa Giliyadi ndi dziko la
Israeli, ku nyanja ya kummawa mpaka ku mzinda wa Tamara. Awa
adzakhala malire akummawa.
19 Mbali yakummwera malire adzayenda kuchokera ku dziwe la mzinda
wa Tamara mpaka ku madzi a ku Meriba Kadesi. Kenaka ndi kutsata
chigwa cha ku Igupto mpaka ku Nyanja Yayikulu. Awa adzakhala
malire akummwera.
20 Mbali ya kumadzulo, malire adzakhala Nyanja Yayikulu mpaka
pa malo oyang'anana ndi Lebo Hamati. Awa adzakhala malire
akumadzulo."

21 "Mugawane dziko limeneli pakati panu potsata mafuko a Israeli.
22 Muligawe kuti likhale cholowa chanu ndiponso cholowa cha alendo
amene akukhala pakati panu, nakhala ndi ana pakati panu. Inu
muwatenge monga mbadwa za mu Israeli. Adzapatsidwe cholowa chawo
pamodzi ndi inu pakati pa mafuko a Israeli. 23 Mu fuko lililonse kumene
mlendoyo akukhala mumupatse cholowa chake." Ndikutero Ine Ambuye
Yehova.

# 48

### *Magawidwe ka Dziko*

1 "Nawa mayina a mafuko a Israeli: Dani adzakhala ndi chigawo
chimodzi kuyambira kumalire akumpoto kuchokera ku nyanja kudzera ku
Hetiloni mpaka ku chipata cha Hamati, kukafika ku Hazari-Enani, mzinda
umene uli kumpoto kwa malire a Damasiko oyang'anana ndi Hamati,
kuchokera m'chigawo chimodzi kummawa mpaka kumadzulo.
2 "Aseri adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi dziko
la Dani kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.
3 "Nafutali adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
dziko la Aseri kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.
4 "Manase adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
dziko la Nafutali kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.
5 "Efereimu adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
dziko la Manase kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.
6 "Rubeni adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
Efereimu kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.
7 "Yuda adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi Rubeni
kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.
8 "Kuchita malire ndi Yuda kuchokera kummawa mpaka kumadzulo
padzakhala chigawo chimene mudzachipereke ngati mphatso ya-
padera. Mulifupi mwake mudzakhala makilomita khumi ndi awiri ndi
theka, ndipo mulitali mwake, kuchokera kummawa mpaka kumadzulo,
mudzafanana ndi zigawo zina za mafuko. Malo a Nyumba ya Mulungu
adzakhala pakati pake.
9 "Chigawo chapadera chimene mudzachipereke kwa Yehova mulitali
mwake mudzakhala makilomita khumi ndi awiri ndi theka ndipo mulifupi
mwake makilomita asanu. 10 Ichi chidzakhala chigawo chopatulika cha
ansembe ndipo chidzagawidwe motere: Mbali ya kumpoto kutalika kwake
kudzakhala makilomita khumi ndi awiri ndi theka, mbali ya kumadzulo
kudzakhala makilomita asanu, mbali ya kummawa makilomita asanu
ndiponso makilomita khumi ndi awiri ndi theka mbali yakummwera.

Pakati pake padzakhala malo a Nyumba ya Mulungu. 11 Chimenechi
chidzakhala chigawo cha ansembe opatulika, ana a Zadoki, amene
ndi okhulupirika ponditumikira Ine, ndipo sanasochere ngati momwe
anachitira Alevi pamene Aisraeli anasochera. 12 Chigawochi, mwa zigawo
zonse za m'dzikomo, chidzakhala kwa ansembewo ngati mphatso yawo
yapadera. Chidzachita malire ndi dziko la Alevi.

13 "Moyandikana ndi chigawo cha ansembe, Alevi adzakhala ndi dera
lawo lotalika makilomita khumi ndi awiri ndi theka, ndipo mulifupi
mwake makilomita asanu. Kutalika kwake konse kudzakhala makilomita
khumi ndi awiri ndi theka ndipo mulifupi mwake makilomita asanu.
14 Asagulitse kapena kusinthitsa mbali iliyonse ya chigawo chimenechi.
Ichi ndi chigawo chabwino kwambiri ndipo chisapatsidwe kwa anthu ena,
chifukwa ndi chopatulikira Yehova.

15 "Chigawo chotsala mulifupi mwake makilomita awiri ndi theka ndipo
mulitali mwake makilomita khumi ndi awiri ndi theka, chidzakhala malo
a anthu wamba, chomangapo nyumba ndiponso chodyetsera ziweto zawo.
Mzinda udzamangidwa pomwepo ndipo udzakhala pakati ndi pakati.
16 Miyeso yake ndi iyi: kumpoto kutalika kwake kudzakhala mamita 2,250,
kummwera mamita 2,250, kummawa mamita 2,250 ndipo kumadzulo
mamita 2,250. 17 Chigawo cha mzinda chodyetsera ziweto chidzakhala
motere: kumpoto kutalika kwake kudzakhala mamita 125, kummwera
kutalika kwake kudzakhala mamita 125, kummawa kutalika kwake
kudzakhala mamita 125, ndipo kumadzulo kutalika kwake kudzakhala
mamita 125. 18 Chigawo chotsala, choyandikana ndi chigawo chopatulika,
kutalika kwake makilomita asanu mbali yakummawa ndiponso makilo-
mita asanu mbali ya kumadzulo. Dera limeneli lidzakhale lolimamo
anthu ogwira ntchito mu mzinda. 19 Anthu ogwira ntchito mu mzinda
amene adzalime m'mundamo adzachokera ku mafuko onse a Israeli.
20 Chigawo chopatulika chonsechi chidzakhale makilomita khumi ndi
awiri ndi theka mbali zonse. Ndiye kuti, mudzapatule padera chigawo
chopatulika pamodzi ndi kadziko ka mzindawo.

21 "Tsono chigawo chotsala pambali zonse ziwiri za chigawo chopatulika
ndi za kadziko ka mzinda, chikhale cha mfumu. Chidzayenda motere:
kuyambira m'malire a chigawo chopatulika kukalekezera m'malire
akummawa. Mbali ina kuyambiranso m'malire a chigawo chopatulika
kukalekezera malire a kumadzulo, kudutsa kufupi ndi zigawo za mafuko.
Dera lonselo likhale la mfumu. 22 Choncho chigawo cha Alevi ndi chigawo
cha mzinda zidzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzayambira mbali ya
kummawa mpaka ya kumadzulo kwa dziko la Benjamini.

23 "Za mafuko ena otsala zidzayenda motere: Benjamini adzakhala
ndi chigawo chimodzi. Chidzayambira mbali ya kummawa mpaka ya
kumadzulo.

24 "Simeoni adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
chigawo cha Benjamini kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.

25 "Isakara adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
chigawo cha Simeoni kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.

26 "Zebuloni adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
chigawo cha Isakara kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.

27 "Gadi adzakhala ndi chigawo chimodzi. Chidzachita malire ndi
chigawo cha Zebuloni kuchokera kummawa mpaka kumadzulo.

28 “Malire a Gadi a mbali yakummwera ku Negevi adzayenda kuchokera
ku Tamara mpaka ku dziwe la Meriba Kadesi komanso kuchokera ku
Mtsinje wa Igupto mpaka ku Nyanja Yayikulu.
29 “Ili ndilo dziko limene mudzagawire mafuko a Israeli kuti likhale
cholowa. Zimenezi zidzakhala zigawo zawo, ndikutero Ine Ambuye
Yehova.

*Zipata za Mzinda*

30 “Izi ndizo zidzakhale zipata zotulukira mzinda, ndipo zidzatchulidwa
mayina a mafuko a Israeli. Kuyambira kumpoto kumene kudzakhala
kotalika mamita 2,250, 31 kudzakhale zipata zitatu izi: cha Rubeni, cha
Yuda ndi cha Levi.
32 “Mbali ya kummawa, imene kutalika kwake ndi mamita 2,250,
kudzakhala zipata zitatu izi: chipata cha Yosefe, chipata cha Benjamini
ndi chipata cha Dani.
33 “Mbali yakummwera, imene kutalika kwake ndi mamita 2,250,
kudzakhala zipata zitatu izi: chipata cha Simeoni, chipata cha Isakara ndi
chipata cha Zebuloni.
34 “Mbali ya kumadzulo, imene kutalika kwake ndi mamita 2,250
kudzakhala zipata zitatu izi: chipata cha Gadi, chipata cha Aseri ndi
chipata cha Nafutali.
35 “Choncho kutalika kwa mzinda kuzungulira kwake kudzakhala
mamita 9,000.

“Ndipo dzina la mzindawo kuyambira nthawi imeneyo mpaka m’tsogolo lidzakhala:

Yehova Ali Pano.”

# Danieli

*Maphunziro a Danieli ku Babuloni*

1 Chaka chachitatu cha ufumu wa Yehoyakimu mfumu ya Yuda,
Nebukadinezara mfumu ya ku Babuloni inabwera ndi kuzinga mzinda
wa Yerusalemu ndi kuwuthira nkhondo. 2 Ndipo Ambuye anapereka
Yehoyakimu mfumu ya ku Yuda m'dzanja lake, pamodzi ndi zina mwa
zida zotumikira m'Nyumba ya Mulungu. Iye anazitenga napita nazo
ku nyumba ya mulungu wake ku Babuloni ndi kuziyika m'nyumba
yosungiramo chuma cha mulungu wake.
3 Tsono mfumu inalamula Asipenazi, mkulu wa nduna zake kuti abwere
nawo ena mwa Aisraeli ochokera m'banja laufumu ndi la olemekezeka,
4 achinyamata wopanda chilema, okongola, aluso mu nzeru zonse, okhala
ndi chidziwitso, achangu pophunzira, odziwa kutumikira m'nyumba
ya mfumu. Ndipo anati awaphunzitsenso kuwerenga chiyankhulo cha
Ababuloni. 5 Ndipo mfumu imawapatsa tsiku ndi tsiku gawo la chakudya
ndi vinyo wa ku nyumba yaufumu, ndi kuti awaphunzitse kwa zaka zitatu,
ndipo kenaka adzayambe kutumikira mfumu.
6 Pakati pa amenewa panali ena ochokera ku Yuda: Danieli, Hananiya,
Misaeli ndi Azariya. 7 Mkulu wa nduna za mfumu anawapatsa mayina at-
sopano: Danieli anamutcha Belitesezara; Hananiya anamutcha Sadirake;
Misaeli anamutcha Mesaki; ndi Azariya anamutcha Abedenego.
8 Koma Danieli anatsimikiza mtima kuti asadzidetse ndi chakudya ndi
vinyo wa mfumu, ndipo anapempha chilolezo kwa mkulu wa nduna za
mfumu kuti asadzidetse mwa njira imeneyi. 9 Ndipo Mulungu anafewetsa
mtima wa ndunayo kuti amukomere mtima ndi kumuchitira chifundo
Danieli, 10 koma ndunayo inamuwuza Danieli kuti, "Ine ndikuchita
mantha ndi mbuye wanga mfumu, amene wapereka chakudya ndi
chakumwa chanu. Kodi akuoneni inu owonda kuposa anzanu a misinkhu
yanu pa chifukwa chanji? Mfumu ikhoza kundidula mutu chifukwa cha
iwe."
11 Ndipo Danieli anati kwa kapitawo amene anali mkulu wa nduna za
mfumu amene anamuyika kuti ayang'anire Danieli, Hananiya, Misaeli ndi
Azariya, 12 "Chonde mutiyese ife akapolo anu pa masiku khumi: mutipatse
masamba okha kuti tidye ndi madzi akumwa. 13 Ndipo mudzafananize
maonekedwe athu ndi a anyamata amene akudya chakudya cha mfumu,
ndi kuti mudzachite ndi anyamata anu monga momwe mudzawaonere."
14 Choncho anawavomera ndipo anawayesa pa masiku khumi.
15 Pakutha pa masiku khumi iwo anaoneka athanzi ndi odya bwino
kuposa aliyense wa anyamata amene ankadya chakudya cha mfumu aja.
16 Choncho kapitawo anawachotsera chakudya ndi vinyo za ku nyumba
yaufumu zija nawapatsa ndiwo zamasamba basi.
17 Kwa anyamata anayiwa Mulungu anapereka chidziwitso ndi
kuzindikira bwino mitundu yonse ya zolembedwa ndi za maphunziro.
Ndipo Danieli ankatanthauzira masomphenya ndi maloto a mitundu
yonse.
18 Ndipo kumapeto kwa masiku amene mfumu inayika kuti adza-
onetse anyamatawa ku nyumba yake, mkulu wa nduna za mfumu uja

anawapereka iwo kwa Nebukadinezara. [19] Mfumu inayankhula nawo,
ndipo panalibe wofanana ndi Danieli; Hananiya Misaeli ndi Azariya;
Choncho analowa ndi kukhala otumikira mfumu. [20] Nthawi zonse mfumu
ikawafunsa zonse zofuna nzeru ndi chidziwitso, inkapeza kuti iwo anali
oposa amatsenga ndi owombeza onse a mu ufumu wake wonse mopitirira
muyeso.

[21] Ndipo Danieli anali kumeneko mpaka chaka choyamba cha ufumu wa
Koresi.

# 2

### *Maloto a Nebukadinezara*

[1] Chaka chachiwiri cha ulamuliro wake, Nebukadinezara analota mal-
oto; anavutika mu mtima mwake ndipo analephera kugona. [2] Tsono
mfumu inayitana amatsenga, owombeza, amawula ndi oyang'ana
nyenyezi kuti amufotokozere zomwe analota. Pamene iwo analowa ndi
kuyima pamaso pa mfumu, [3] mfumuyo inawawuza kuti, "Ndalota loto
lomwe likundisautsa ndipo ndikufuna kudziwa tanthauzo lake."

[4] Pamenepa alawuli anati kwa mfumu m'Chiaramu, "Mukhale ndi
moyo wautali mfumu! Tiwuzeni ife atumiki anu zimene mwalota, ndipo
tidzakuwuzani tanthauzo lake."

[5] Mfumu inayankha alawuliwo kuti, "Zimene ndatsimikiza kuchita
ndi izi: Ngati inu simundifotokozera zimene ndalota ndi tanthauzo
lake, mudzadulidwa nthulinthuli ndipo nyumba zanu ndidzazisandutsa
bwinja. [6] Koma ngati mundiwuza zimene ndalota ndi tanthauzo lake,
ndidzakupatsani mphatso ndi mphotho ndi ulemu waukulu. Choncho
mundiwuze zimene ndalota ndi tanthauzo lake."

[7] Iwo anayankhanso kachiwiri kuti, "Mfumu iwuze atumiki ake chimene
yalota, ndipo ife tidzatanthauzira."

[8] Ndipo mfumu inayankha kuti, "Ine ndikudziwa kuti mukungozen-
gereza kufuna kutaya nthawi chabe chifukwa mukuzindikira kuti izi ndi
zimene ndatsimikiza kuchita. [9] Ngati simundiwuza zimene ndalota, chi-
lango chake ndi chimodzi. Inu mwagwirizana kuti mundiwuze ine bodza
ndi chinyengo ndi kuyembekeza kuti ine ndisintha. Tsono mundiwuze
zimene ndalota, ndipo ine ndidzadziwa kuti mukhoza kunditanthauzira."

[10] Alawuli anayankha mfumu kuti, "Palibe munthu pa dziko lapansi
amene akhoza kuchita chimene mfumu ikufunsa! Palibe mfumu,
kaya yayikulu kapena yamphamvu bwanji imene inafunsapo amatsenga,
owombeza kapena alawuli aliwonse zimenezi. [11] Zimene mfumu yafunsa
ndi zapatali. Palibe wina amene angathe kuwulula izi kwa mfumu
kupatula milungu, ndipo sikhala pakati pa anthu."

[12] Zimenezi zinapsetsa mtima mfumu ndipo inakwiya kwambiri kotero
inalamula kuti anzeru onse a ku Babuloni aphedwe. [13] Choncho
lamulo linaperekedwa kuti anthu anzeru aphedwe, ndipo anatuma anthu
kukafunafuna Danieli ndi anzake kuti iwonso aphedwe.

[14] Danieli anayankhula mwanzeru ndi mwaulemu kwa Ariyoki, mkulu
wa asilikali olondera mfumu amene anatumidwa kukapha anthu anzeru
a ku Babuloni. [15] Danieli anafunsa Ariyoki kapitawo wa mfumu kuti,
"Chifukwa chiyani mfumu yapereka lamulo lankhanza lotere?" Kenaka
Ariyoki anafotokoza nkhaniyi kwa Danieli. [16] Danieli anapita mofulumira

kwa mfumu ndipo anamupempha kuti amupatse nthawi kuti amuwuze
zimene walota ndi tanthauzo lake.
[17] Kenaka Danieli anabwerera ku nyumba kwake ndi kukafotokozera
anzake aja zimenezi: Hananiya, Misaeli ndi Azariya. [18] Danieli anadan-
daulira anzake kuti apemphe kwa Mulungu wakumwamba kuti awachitire
chifundo ndi kumuwululira chinsinsi, kuti iye ndi anzakewo asany-
ongedwe pamodzi ndi anzeru ena onse a ku Babuloni. [19] Usiku Yehova
anamuwululira Danieli chinsinsi chija m'masomphenya. Pamenepo
Danieli anatamanda Mulungu wakumwamba, [20] ndipo anati:
"Litamandike dzina la Mulungu ku nthawi za nthawi;
nzeru ndi mphamvu zonse ndi zake.
[21] Amasintha nthawi ndi nyengo;
amakweza mafumu ndipo amawatsitsanso.
Amapatsa nzeru kwa anzeru
ndi chidziwitso kwa ozindikira zinthu.
[22] Amavumbulutsa zinthu zozama ndi zobisika;
amadziwa zimene zili mu mdima,
ndipo kuwunika kumakhala ndi Iye.
[23] Ndikuyamika ndi kutamanda Inu Mulungu wa makolo anga:
mwandipatsa nzeru ndi mphamvu,
mwandiwululira zomwe tinakupemphani,
mwatiwululira maloto a mfumu."

### *Danieli Atanthauzira Maloto*

[24] Motero Danieli anapita kwa Ariyoki, amene mfumu inamusankha kuti akaphe anthu anzeru a ku Babuloni, ndipo anati kwa iye, "Musaphe anthu anzeru a ku Babuloni. Ndiperekezeni kwa mfumu, ndipo ndidzayimasulira maloto ake."

[25] Ariyoki anapita naye Danieli kwa mfumu nthawi yomweyo ndipo anati, "Ndapeza munthu pakati pa akapolo ochokera ku Yuda amene akhoza kuwuza mfumu zimene maloto ake akutanthauza."

[26] Mfumu inafunsa Danieli (wotchedwanso Belitesezara) kuti, "Kodi ukhoza kundiwuza zomwe ine ndinaona m'maloto anga ndi tanthauzo lake?"

[27] Danieli anayankha kuti, "Palibe munthu wanzeru, wowombeza,
wamatsenga kapena wamawula amene akhoza kufotokozera mfumu
chinsinsi chimene mwafuna kudziwa, [28] koma kuli Mulungu kumwamba
amene amawulula zinsinsi. Iye waonetsera mfumu Nebukadinezara
zimene zidzachitika m'masiku akutsogolo. Maloto ndi masomphenya anu
amene munawaona mukugona pa bedi lanu ndi awa:
[29] "Mukugona pa bedi, inu Mfumu, maganizo anakufikirani a zinthu
zakutsogolo, ndipo Yehova wowulula zinsinsi anakuonetserani zimene
zidzachitika. [30] Koma chinsinsi ichi chavumbulutsidwa kwa ine, si
chifukwa chakuti ndili ndi nzeru zochuluka kuposa anthu ena onse, koma
kuti mfumu mudziwe tanthauzo la maloto anu ndi kuti muzindikire
maganizo amene anali mu mtima mwanu.
[31] "Inu mfumu, munaona chinthu chowumba chachikulu chimene
chinayima pamaso panu. Chowumbachi chinali chonyezimira
m'maonekedwe. [32] Mutu wa chowumbacho unali wagolide wabwino
kwambiri. Chifuwa ndi manja ake zinali zasiliva. Mimba ndi ntchafu
zake zinali zamkuwa. [33] Miyendo yake inali yachitsulo, mapazi ake anali
achitsulo chosakaniza ndi dongo. [34] Inu mukuona, mwala unagamuka,

koma osati ndi manja a munthu. Unagwera fanolo pa mapazi ake achitsulo
chosakaniza ndi dongo aja ndi kuwaphwanya. 35 Tsono chitsulo, dongo,
mkuwa, siliva ndi golide zonse zinaphwanyika pamodzi ndikukhala
tizidutswa towuluka ndi mphepo ngati mungu wa mowombera tirigu
nthawi ya chilimwe. Zonse zinawuluka ndi mphepo osasiyako chilichonse.
Koma mwala umene unagwera pa chowumba chija unasanduka phiri
lalikulu ndi kudzaza dziko lonse lapansi.

36 “Maloto aja ndi amenewa; tidzafotokoza tanthauzo lake kwa mfumu.
37 Inu mfumu, ndinu mfumu ya mafumu. Mulungu wakumwamba
wakupatsani ufumu, ulamuliro ndi mphamvu ndi ulemerero; 38 Iye
anayika m’manja mwanu anthu ndi nyama zakuthengo ndi mbalame
zamlengalenga. Kulikonse kumene zikhala, iye anakuyikani wolamulira
wa zonse. Inu ndinu mutu wagolidewo.

39 “Pambuyo pa inu, ufumu wina udzadzuka, wochepa mphamvu
poyerekeza ndi wanuwu. Padzabweranso ufumu wachitatu, wamkuwa,
udzalamulira dziko lonse lapansi. 40 Pomaliza, padzakhala ufumu
wachinayi, wolimba ngati chitsulo popeza chitsulo chimaphwanya ndi
kutikita chilichonse. Ndipo monga chitsulo chimaphwanya zinthu
ndikuteketeratu, choncho udzawononga ndi kuphwanya maufumu ena
onse. 41 Ndipo monga munaonera kuti mapazi ndi zala zake zinali
za chitsulo chosakaniza ndi dongo, choncho uwu udzakhala ufumu
wogawikana; komabe udzakhala ndi mphamvu zina zachitsulo zotikita.
42 Monga zala zinali za chitsulo chosakaniza ndi dongo, choncho ufumu
uwu udzakhala pang’ono wolimba ndi pang’ono wofowoka. 43 Ndipo
monga munaona chitsulo chosakanizidwa ndi dongo, choncho anthu
adzakhala wosakanizana ndipo sadzagwirizana, monga muja chitsulo
sichingasakanizike ndi dongo.

44 “Pa nthawi ya mafumu amenewo, Mulungu wakumwamba adzak-
hazikitsa ufumu umene sudzawonongedwa, kapenanso kuperekedwa kwa
anthu ena. Udzawononga maufumu onse aja ndi kuwatheratu, koma iwo
wokha udzakhalapobe mpaka muyaya. 45 Limeneli ndilo tanthauzo la
masomphenya a mwala umene unagamuka pa phiri, koma osati ndi manja
a anthu; mwala umene unaphwanya chitsulo, mkuwa, dongo, siliva ndi
golide m’tizidutswa.

“Mulungu wamkulu wakuonetsani mfumu chimene chidzachitika kutsogolo. Malotowo ndi woona ndipo tanthauzo lake ndi lodalirika.”

46 Pamenepo mfumu Nebukadinezara inadzigwetsa chafufumimba pa-
maso pa Danieli ndi kumupatsa ulemu. Ndipo inalamula kuti anthu onse
amuthirire Danieli nsembe ndi kumufukizira lubani. 47 Mfumu inati kwa
Danieli, “Zoonadi, Mulungu wako ndi Mulungu wa milungu ndi Ambuye
wa mafumu ndi wowulula zinsinsi, pakuti iwe wathadi kuwulula chinsinsi
ichi.”

48 Ndipo mfumu inamukweza Danieli ndi kumupatsa mphatso zambiri.
Anamuyika kuti akhale wolamulira chigawo chonse cha Babuloni ndi
kutinso akhale woyang’anira anthu ake onse anzeru. 49 Komanso,
monga mwa pempho la Danieli, mfumu inayika Sadirake, Mesaki ndi
Abedenego, kuti akhale oyang’anira chigawo cha Babuloni, pamene
Danieliyo ankakhazikika m’bwalo la mfumu.

# 3

*Fano la Golide ndi Ng’anjo ya Moto*

1 Mfumu Nebukadinezara anapangitsa fano la golide lotalika mamita
27 ndi mulifupi mwake mamita atatu, ndipo analiyimika m'chigwa cha
Dura m'chigawo cha Babuloni. 2 Kenaka iye anayitanitsa akalonga,
abwanamkubwa, nduna, aphungu, asungichuma, oweruza milandu,
anyakwawa ndi akulu ena onse a madera a dzikolo, kuti abwere ku
mwambo wotsekula fano limene analiyimika lija. 3 Choncho akalonga,
abwanamkubwa, nduna, aphungu, asungichuma, oweruza milandu,
anyakwawa, ndi akulu ena onse a madera a dzikolo, anasonkhana
kudzachita mwambo wotsekulira fano limene mfumu Nebukadinezara
analiyimika, ndipo mlaliki anayimirira pamaso pa fanolo nati:

4 "Inu anthu a mitundu yonse ndi a ziyankhulo zonse, mukulamulidwa
kuti muchite izi: mitundu ya anthu ndi a chiyankhulo chilichonse
5 mukadzamva kulira kwa lipenga, chitoliro, zeze, sansi, chisakasa, mngoli
ndi nyimbo za mtundu uliwonse, muyenera kulambira ndi kupembedza
fano la golide limene mfumu Nebukadinezara analiyimika. 6 Aliyense
amene sadzalambira ndi kupembedza adzaponyedwa nthawi yomweyo
m'ng'anjo ya moto."

7 Choncho anthu onse aja atangomva kulira kwa lipenga, chitoliro, zeze,
sansi, chisakasa, mngoli ndi nyimbo za mtundu uliwonse, analambira ndi
kupembedza fano la golide limene mfumu Nebukadinezara analiyimika.

8 Pa nthawi imeneyi alawuli ena anafika ndi kuwanenera zoyipa Ayuda.
9 Iwo anati kwa mfumu Nebukadinezara, "Inu mfumu mukhale ndi moyo
wautali! 10 Inu mfumu, mwakhazikitsa lamulo kuti aliyense akamva
kulira kwa lipenga, chitoliro, zeze, sansi, chisakasa, mngoli ndi nyimbo
za mtundu uliwonse, ayenera kulambira ndi kupembedza fano la golide,
11 ndi kuti aliyense osalambira ndi kupembedza adzaponyedwa m'ng'anjo
ya moto. 12 Koma alipo Ayuda ena Sadirake, Mesaki ndi Abedinego amene
munawayika kuti ayang'anire ntchito ya dera la ku Babuloni. Anthu
amenewa sakumvera inu mfumu. Iwo sakutumikira milungu yanu kapena
kulambira fano la golide limene munaliyimikalo."

13 Tsono Nebukadinezara anakwiya ndi kupsa mtima kwambiri, ndipo
anayitanitsa Sadirake, Mesaki ndi Abedenego. Choncho amuna awa anab-
wera pamaso pa mfumu, 14 ndipo Nebukadinezara anawafunsa kuti, "Kodi
ndi zoona, Sadirake, Mesaki ndi Abedenego, kuti simukutumikira milungu
yanga kapena kupembedza fano la golide ndinaliyikalo? 15 Tsopano
ngati muli okonzeka kulambira ndi kupembedza fano ndinalipanga,
mukangomva kulira kwa lipenga chitoliro, zeze, sansi, chisakasa, mngoli
ndi nyimbo za mtundu uliwonse, muchita bwino. Koma ngati simulipem-
bedza, mudzaponyedwa m'nganjo ya moto. Nanga ndi mulungu uti amene
adzatha kukupulumutsani m'manja anga?"

16 Sadirake, Mesaki ndi Abedenego anayankha mfumu Nebukadinezara
kuti, "Sikoyenera kuti tikuyankheni pa nkhani imeneyi. 17 Ngati
tiponyedwa m'ng'anjo ya moto, Mulungu amene timamutumikira akhoza
kutipulumutsa ku ng'anjo yamotoyo, ndipo adzatilanditsa m'dzanja lanu
mfumu. 18 Koma ngakhale Mulungu wathu atapanda kutipulumutsa,
tikufuna mudziwe inu mfumu, kuti sitidzatumikira milungu yanu kapena
kupembedza fano la golide limene munaliyimika."

19 Pamenepo Nebukadinezara anapsa mtima ndi Sadirake, Mesaki ndi
Abedenego, ndipo anayipidwa nawo. Iye analamulira kuti ng'anjo
ayitenthetse kasanu ndi kawiri kuposa nthawi zonse, 20 ndipo analamula
ena mwa asilikali amphamvu kwambiri m'gulu lake lankhondo kuti

amange Sadirake, Mesaki ndi Abedenego ndi kuwaponya m'ng'anjo ya
moto. 21 Choncho amuna awa, atavala mikanjo yawo, mabuluku, nduwira
ndi zovala zina zonse, anamangidwa ndi kuponyedwa m'ng'anjo ya
moto. 22 Tsono popeza lamulo la mfumu linali lofulumiza, ng'anjo
inatenthetsedwa kowirikiza mwakuti malawi ake anapha asilikali amene
ananyamula Sadirake, Mesaki ndi Abedenego, 23 ndipo anyamata atatuwa,
ali chimangidwire, anagwera m'ng'anjo ya moto.

24 Kenaka mfumu Nebukadinezara anadabwa ndipo anafunsa nduna
zake kuti, "Kodi sanali amuna atatu amene anamangidwa ndi
kuponyedwa m'moto?"

Iwo anayankha kuti, "Ndi zoonadi, mfumu."

25 Iye anati, "Taonani! Ndikuona amuna anayi akuyendayenda
m'moto, osamangidwa ndi osapwetekedwa ndipo wachinayi akuoneka
ngati mwana wa milungu."

26 Pamenepo Nebukadinezara anayandikira pa khomo lang'anjo ya moto
ndi kufuwula kuti, "Sadirake, Mesaki ndi Abedenego, atumiki a Mulungu
Wammwambamwamba, tulukani! Bwerani kuno!"

Ndipo Sadirake, Mesaki ndi Abedenego anatuluka m'moto, 27 ndipo
akalonga, akazembe, abwanamkubwa ndi nduna zamfumu anasonkhana
mowazungulira. Anaona kuti moto sunatenthe matupi awo ngakhale tsitsi
kumutu kwawo silinapse; zovala zawo sizinapse, ndipo sankamveka fungo
la moto.

28 Kenaka Nebukadinezara anati, "Atamandike Mulungu wa Sadirake,
Mesaki ndi Abedenego, amene anatumiza mngelo wake ndi kupulumutsa
atumiki ake! Iwo anakhulupirira Iye ndi kunyozera lamulo la mfumu
ndipo anali okonzeka kutaya moyo wawo koposa kutumikira kapena
kupembedza mulungu wina aliyense wosakhala Mulungu wawo. 29 Tsono
ndikulamula kuti anthu a mitundu ina kaya chiyankhulo china chili
chonse amene anganyoze Mulungu wa Sadirake, Mesaki ndi Abedenego
adulidwe nthulinthuli ndipo nyumba zawo ndidzagwetsa ndi kusandutsa
bwinja, popeza palibe Mulungu amene akhoza kupulumutsa m'njira
yotere."

30 Ndipo mfumu Nebukadinezara anakweza pa ntchito Sadirake, Mesaki
ndi Abedenego m'chigawo cha Babuloni.

# 4

*Maloto Achiwiri a Nebukadinezara*

1 Mfumu Nebukadinezara anatumiza mawu awa kwa anthu a mitundu
yonse, ndi chiyankhulo chilichonse, amene amakhala pa dziko lonse
lapansi:

Mtendere uchuluke pakati panu!

2 Chandikomera kukuwuzani zizindikiro zozizwitsa ndi zodabwitsa
zimene Mulungu Wammwambamwamba wandichitira.

3 Zizindikiro zake ndi zazikulu,
zozizwitsa zake ndi zamphamvu!
Ufumu wake ndi wamuyaya;
ulamuliro wake ndi wa mibadomibado.

4 Ine Nebukadinezara, ndinali kwathu m'nyumba yanga yaufumu,
mwa mtendere ndipo ndinali wokhutitsidwa. 5 Ndili chigonere pa
bedi langa, ndinalota maloto amene anandichititsa mantha. Zinthu ndi

masomphenya zimene ndinaziona zinandiopsa. 6 Choncho ndinalamula
kuti anthu onse a nzeru a ku Babuloni abwere pa maso panga
kunditanthauzira malotowo. 7 Pamene amatsenga, owombeza, alawuli
ndi amawula anabwera, ndinawafotokozera maloto, koma sanathe
kunditanthauzira. 8 Potsiriza, anabwera Danieli uja amatchedwa
Belitesezara, potsata dzina la mulungu wanga, ndipo mzimu wa milungu
yoyera uli mwa iye. Iyeyu ndinamufotokozera malotowo.
9 Ndinati, "Belitesezara, mkulu wa amatsenga, ndikudziwa kuti mzimu
wa milungu yoyera uli mwa iwe, ndipo palibe chinsinsi chomwe
sungachidziwe. Awa ndi maloto anga; unditanthauzire. 10 Awa ndi
masomphenya amene ine ndinaona pamene ndinali kugona pa bedi:
Ndinaona, mtengo wautali kwambiri utayima pakati pa dziko lapansi.
11 Mtengowo unakula ndi kulimba ndipo msonga yake inafika mpaka
mlengalenga; umaonekera pa dziko lonse lapansi. 12 Masamba ake
anali okongola, zipatso zinali zochuluka, ndipo mu mtengomo munali
chakudya chokwanira anthu onse. Zirombo zakuthengo zimapeza
mthunzi m'munsi mwake, ndipo mbalame zamlengalenga zimakhala pa
nthambi zake: Cholengedwa chilichonse chinkadya za mu mtengowu.
13 "Ndikanali chigonere ndinaona m'masomphenya mngelo atayima
pamaso panga, woyera, atatsika kuchokera kumwamba. 14 Anayankhula
mofuwula kuti, 'Gwetsa mtengo ndi kusadza nthambi zake; yoyola
masamba ake kuti nyama zakuthengo zithawe pa mthunzi pake ndi
mbalame zithawe pa nthambi zake. 15 Koma musiye tsinde ndi mizu
yake m'nthaka. Tsindelo mulimange maunyolo a chitsulo ndi mkuwa,
zikhalebe m'nthaka, n'kudya udzu m'munda.
" 'Mumulole iye anyowe ndi mame akumwamba, ndipo iye akhale ndi
nyama pakati pa zomera za m'nthaka. 16 Maganizo ake a umunthu
asinthidwe ndipo apatsidwe maganizo a nyama ya kuthengo, mpaka
zaka zisanu ndi ziwiri zitadutsa.
17 " 'Angelo oyera ndiwo akutsimikiza chilangochi. Tsono anthu
adziwe kuti Mulungu Wammwambamwamba ali ndi mphamvu yola-
mulira maufumu onse, ndipo amawapereka kwa aliyense akumufuna,
ngakhale munthu wamba kuti alamulire.'
18 "Amenewa ndi maloto amene ine, mfumu Nebukadinezara, ndi-
nalota. Tsopano Belitesezara, undifotokozere tanthauzo lake, popeza
palibe mwa anthu anzeru a mu ufumu wanga amene angathe kundi-
tanthauzira. Koma iwe ukhoza, chifukwa mzimu wa milungu yoyera uli
mwa iwe."

### *Danieli Atanthauzira Maloto*

19 Pamenepo Danieli, amene amatchedwa Belitesezara, anavutika
mu mtima kwambiri kwa kanthawi, ndipo anasautsidwa m'maganizo
ake. Choncho mfumu inati, "Belitesezara usalole malotowa kapena
tanthauzo lake likuopse."
Belitesezara anayankha kuti, "Mbuye wanga, ndikanakonda mal-
otowa akanakhudza adani anu okha, ndi tanthauzo lake kwa iwo
okusautsani! 20 Mtengo munawuona uja, umene unkakulirakulira
kwambiri ndi kulimba, ndi msonga yake inafika mlengalenga, ndi
kuonekera ku dziko lonse lapansi, 21 mtengo umene masamba ake anali
okongola ndiponso unali ndi zipatso zochuluka zokwanira kudya anthu
onse a dziko lapansi. Mtengowu unkapereka mthunzi ku zirombo zonse
zakuthengo, ndipo mbalame zamlengalenga zinayika zisa pa nthambi
zake. 22 Inu mfumu, ndinu mtengo umenewo! Inu mwakhala wamkulu

ndi wamphamvu; ukulu wanu wakula mpaka wakhudza mlengalenga,
ndipo ufumu wanu wafika mpaka ku malo akutali a dziko lapansi.
23 “Inu mfumu munaona mthenga woyera, akuchokera kumwamba
ndipo anati, ‘Gwetsani mtengo ndipo muwuwononge, koma musiye
tsinde ndi mizu yake. Tsindelo mulimange ndi unyolo wa chitsulo
ndi mkuwa ndipo mulisiye pakati pa udzu wa m’munda. Mulole kuti
linyowe ndi mame akumwamba. Likhale ngati nyama zakuthengo,
mpaka zaka zidutse zisanu ndi ziwiri.’
24 “Tanthauzo lake ndi ili mfumu, izi ndi zimene Mulungu
Wammwambamwamba watsimikiza kuti zikugwereni mbuye wanga
mfumu: 25 Inu mudzachotsedwa pakati pa anthu ndipo mudzakhala
ndi nyama zakuthengo; mudzadya udzu monga ng’ombe ndi kunyowa
ndi mame akumwamba. Zaka zisanu ndi ziwiri zidzadutsa mpaka
mudzavomereze kuti Mulungu Wammwambamwamba ndiye mwini
ulamuliro pa ma ufumu a anthu, ndipo amawapereka kwa aliyense
amene Iye wafuna. 26 Lamulo losiya tsinde la mtengo ndi mizu yake
litanthauza kuti ufumu wanu udzabwezeredwa kwa inu mukadza-
vomereza kuti Mulungu ndiye amalamulira. 27 N’chifukwa chake
mfumu, chikukomereni kulandira malangizo anga: Lekani machimo
ndipo muzichita zabwino, lekani mphulupulu zanu ndipo muzikomera
mtima anthu opsinjika. N’kutheka kuti mtendere wanu udzapitirira.”

### *Maloto Akwaniritsidwa*

28 Zonsezi zinamuchitikira mfumu Nebukadinezara. 29 Itapita miyezi
khumi ndi iwiri, pamene mfumu inkayenda pa denga la nyumba
ya ufumu ya ku Babuloni, 30 iye anati, “Kodi Babuloni si mzinda
wamphamvu ndi wokongola umene ndinamanga ndi mphamvu zanga
ngati nyumba yanga yaufumu, kuonetsera ulemerero wa ufumu
wanga?”
31 Akuyankhulabe izi mawu anamveka kuchokera kumwamba kuti,
“Imvani izi, mfumu Nebukadinezara: Ufumu wako wachotsedwa.
32 Udzachotsedwa pakati pa anthu ndipo udzakhala ndi zirombo
zakuthengo; udzadya udzu monga ng’ombe. Zaka zisanu ndi ziwiri
zidzadutsa mpaka iwe utavomereza kuti Wammwambamwamba ndiye
mwini ulamuliro pa maufumu a anthu ndipo amawupereka kwa
aliyense amene iye afuna.”
33 Nthawi yomweyo zonse zimene zinanenedwa zokhudza
Nebukadinezara zinakwaniritsidwa. Iye anachotsedwa pakati pa
anthu ndipo ankadya udzu ngati ng’ombe. Thupi lake linanyowa
ndi mame akumwamba mpaka tsitsi lake linakula ngati nthenga za
chiwombankhanga ndi zikhadabo ngati zikhadabo za mbalame.

34 Pomaliza pa zaka zimenezo ine, Nebukadinezara ndinakweza
maso anga kumwamba, ndipo nzeru zanga zinabwereramo. Kenaka
ndinatamanda Wammwambamwamba; ndinamupatsa ulemu ndi ku-
mulemekeza Iye amene akhala nthawi zonse.
Ulamuliro wake ndi ulamuliro wa nthawi zonse;
ufumu wake udzakhala ku mibadomibado.
35 Anthu onse a dziko lapansi
ali chabe pamaso pake.
Pakati pa angelo akumwamba
ndi anthu a dziko lapansi
palibe amene akhoza kumuletsa

Mulungu kuchita zimene afuna.
Kapena kunena kwa Iye kuti, “Kodi mwachita chiyani?”
36 Pa nthawi yomweyo nzeru zanga zinabwereramo. Ndinalandi-
ranso ulemu wanga ndi ufumu wanga. Nduna ndi akalonga anga
anandilandiranso. Ndipo anandibwezera ufumu wanga ndi kukhalanso
wamphamvu kuposa kale. 37 Tsopano ine Nebukadinezara, ndikuta-
manda, kukweza ndi kulemekeza Mfumu yakumwamba chifukwa zonse
zimene amachita ndi zoyenera ndipo njira zake zonse ndi zachilungamo.
Ndipo onse amene amayenda modzikuza adzawatsitsa.

# 5

*Malemba pa Khoma*

1 Tsiku lina mfumu Belisazara anakonza phwando lalikulu la akalonga
ake 1,000 ndipo anamwa vinyo pamodzi ndi iwo. 2 Pamene Belisazara
ankamwa vinyo, analamula kuti ziwiya zagolide ndi zasiliva zimene
Nebukadinezara abambo ake anakatenga m'Nyumba ya Mulungu ku
Yerusalemu zikatengedwe kuti mfumu ndi akalonga ake, akazi ake ndi
azikazi amweremo. 3 Choncho anabweretsa ziwiya zagolide zimene
anazitenga m'Nyumba ya Mulungu; ndipo mfumu ndi akalonga ake, akazi
ake ndi azikazi ake anamweramo. 4 Akumwa vinyo, anatamanda milungu
yagolide ndi siliva, yamkuwa, chitsulo, yamtengo ndi mwala.
5 Mwadzidzidzi zala za dzanja la munthu zinaonekera ndi kulemba
pa khoma, pafupi ndi choyikapo nyale m'nyumba yaufumu. Mfumu
inapenyetsetsa dzanjalo pamene limalemba. 6 Nkhope yake inasandulika
ndipo inachita mantha, nkhongono zii, mawondo gwedegwede.
7 Mfumu inafuwula kuyitana owombeza, alawuli ndi amawula kuti
abwere. Ndipo anawawuza anthu anzeru a ku Babuloni kuti, “Aliyense
amene awerenge malembawa ndi kundiwuza tanthauzo lake adza-
vekedwa chovala cha pepo ndi mkanda wa golide udzavekedwa m'khosi
mwake, ndipo adzakhala wolamulira wachitatu mu ufumuwu.”
8 Pamenepo anzeru onse a mfumu anabwera, koma sanakwanitse
kuwerenga malembawo kapena kumutanthauzira mfumu. 9 Choncho
mfumu Belisazara anachita mantha koposa ndipo nkhope yake inapitirira
kusinthika. Akalonga ake anathedwa nzeru.
10 Mfumukazi, pakumva mawu a mfumu ndi akalonga ake, analowa
m'chipinda cha phwando ndipo anati, “Mfumu mukhale ndi moyo
wautali! Musavutike! Nkhope yanu isasinthike! 11 Pali munthu wina
mu ufumu wanu uno amene mwa iye muli mzimu wa milungu yoyera.
Pa nthawi ya ulamuliro wa abambo anu iye anapezeka kuti ali ndi
chidziwitso, luntha ndi nzeru zonga za milungu. Mfumu Nebukadinezara,
abambo anu, Ine ndikukuwuzani anamusankha iye kukhala mkulu wa
amatsenga, owombeza, alawuli ndi amawula. 12 Munthu ameneyu dzina
lake ndi Danieli, koma mfumu inamutcha Belitesezara ndipo ali ndi
nzeru zapadera, ndi wodziwa ndi kuzindikira zinthu, ndiponso luso
lakutanthauzira maloto, kufotokozera miyambi ndi kuthetsa mavuto
osautsa. Muyitaneni Danieli, ndipo adzakuwuzani chomwe mawuwa
akutanthauza.”
13 Choncho anabwera naye Danieli pamaso pa mfumu ndipo inati kwa
iye, “Kodi ndiwe Danieli, mmodzi mwa akapolo omwe abambo anga
mfumu anabwera nawo kuchoka ku Yuda? 14 Ndamva kuti mzimu wa

milungu uli mwa iwe ndi kuti uli ndi chidziwitso, luntha ndi nzeru za-
padera. 15 Anzeru ndi owombeza anabwera pamaso panga kuti awerenge
zolembedwazi ndi kundiwuza tanthauzo lake koma sanakwanitse kundi-
fotokozera. 16 Tsopano ndamva kuti iwe ukhoza kupereka matanthauzo
ndi kuthetsa mavuto. Ngati ungawerenge zolembedwazi ndi kundiwuza
tanthauzo lake, udzavekedwa chovala cha pepo ndi kuyikidwa mkanda wa
golide m'khosi mwako, ndipo udzakhala wolamulira wachitatu mu ufumu
uno."

17 Pamenepo Danieli anayankha mfumu kuti, "Inu musunge mphatso
zanuzo kwa inu nokha ndipo mupereke mphothoyo kwa wina aliyense.
Komabe ine ndi kuwerengerani malembawa mfumu; ndikukuwuzani
tanthauzo lake.

18 "Inu mfumu, Mulungu Wammwambamwamba anapatsa abambo
anu Nebukadinezara mphamvu ndi ukulu ndi ulemerero ndi ufumu.
19 Chifukwa cha udindo waukulu umene anapatsidwanso, anthu onse
ndi mitundu ndi anthu aziyankhulo zosiyanasiyana ankanjenjemera
ndikumuopa iye. Amene mfumu inafuna anawaphadi; amene inafuna
kuwasunga, inawasunga; amene inafuna kuwakweza, inawakweza; ndipo
amene inafuna kuwatsitsa, inawatsitsa. 20 Koma pamene inayamba kudzi-
tama ndi kuwumitsa mtima wake ndi kuyamba kunyada, inachotsedwa
pa mpando wake waufumu ndi kulandidwa ulemerero wake. 21 Iyo
inachotsedwa pakati pa anthu ndi kupatsidwa mtima ngati wa nyama;
inakhala pamodzi ndi abulu akutchire ndi kudya udzu ngati ng'ombe;
ndipo thupi lake linanyowa ndi mame akumwamba, mpaka pamene
anavomereza kuti Mulungu Wammwambamwamba ndiye wolamulira
maufumu a anthu ndipo amawupereka kwa aliyense amene Iye wafuna.

22 "Koma inu mwana wake, Belisazara, simunadzichepetse, ngakhale
kuti mumadziwa zonsezi. 23 M'malo mwake, mwadzikweza nokha kut-
sutsana ndi Ambuye wakumwamba. Inu mwatenga ziwiya za m'Nyumba
mwake, ndipo inu ndi akalonga anu, akazi anu ndi azikazi anu mwamwera
vinyo mu zimenezi. Inu munatamanda milungu yasiliva ndi golide,
yamkuwa, chitsulo, mtengo ndi mwala, imene singaone kapena kumva
kapena kuzindikira. Koma simunamupatse ulemu Mulungu amene asunga
m'manja mwake moyo wanu ndi njira zanu zonse. 24 Choncho Iye
watumiza dzanja limene lalemba mawu amenewa.

25 "Mawu amene analembedwa ndi awa:

MENE, MENE, TEKELI, PARASINI.

26 "Zimene mawuwa akutanthauza ndi izi:

Mene: Mulungu wawerenga masiku a ufumu wanu ndipo wauthetsa.

27 Tekeli: Inu mwayesedwa pa sikelo ndipo mwapezeka kuti muku-
perewera.

28 Parasini: Ufumu wanu wagawidwa ndi kupatsidwa kwa Amedi ndi
Aperezi."

29 Mwa lamulo la Belisazara, Danieli anavekedwa chovala cha pepo,
mkanda wagolide unayikidwa m'khosi mwake, ndipo analengeza kuti
anali wachitatu mu ulamuliro mu ufumuwo.

30 Usiku womwewo Belisazara, mfumu ya anthu a ku Babuloni,
inaphedwa, 31 ndipo Dariyo Mmedi analanda ufumuwo ali ndi zaka 62.

# 6

### *Danieli M'dzenje la Mikango*

1 Kunamukomera Dariyo kusankha akalonga 120 kuti alamulire mu
ufumu wonse, 2 ndikusankha nduna zazikulu zitatu kuti ziwayang'anire
ndipo imodzi mwa ndunazo anali Danieli. Akalongawo amayang'aniridwa
ndi nduna zazikuluzo kuti zinthu za mfumu zisawonongeke. 3 Tsono
Danieli anadzionetsa kuti akhoza kugwira ntchito bwino kopambana
nduna zinzake chifukwa anali wanzeru kwambiri. Ndiye mfumu ina-
ganiza zomuyika kuti akhale woyang'anira ufumu wonse. 4 Chifukwa cha
ichi, anzake ndi akalonga anayesa kupeza zifukwa zomutsutsira Danieli
pa kayendetsedwe ka ntchito za dzikolo, koma sanapeze cholakwa chili-
chonse. Iwo sanapeze chinyengo mwa iye, chifukwa anali wokhulupirika
ndipo sankachita chinyengo kapena kutayirira ntchito. 5 Pomaliza,
anthu awa ananena kuti, “Sitidzapeza cholakwa chilichonse chomutsut-
sira Danieli kupatula chokhacho chimene chikhudza chipembedzo cha
Mulungu wake.”

6 Choncho akalonga ndi nduna pamodzi anapita kwa mfumu ndipo
anati: “Inu mfumu Dariyo, mukhale ndi moyo wautali! 7 Nduna
zoyendetsa ufumu wanu, aphungu, akalonga ndi abwanamkubwa tonse
tagwirizana kuti inu mfumu mukhazikitse lamulo ndi kulisindikiza kuti
aliyense amene apemphera kwa mulungu wina kapena kwa munthu
kupatula kwa inu mfumu, pa masiku makumi atatu otsatirawa, adza-
ponyedwa m'dzenje la mikango. 8 Tsopano inu mfumu khazikitsani
lamulo limeneli ndipo musindikizepo dzina lanu kuti lisasinthike monga
mwa malamulo a Amedi ndi Aperezi, amene sasinthidwa.” 9 Choncho
mfumu Dariyo anasindikizapo dzina lake pa lamuloli.

10 Danieli atamva kuti lamulo lasindikizidwa, anapita ku nyumba kwake
nalowa m'chipinda chapamwamba chimene mazenera ake anali otsekula
kuloza ku Yerusalemu. Katatu pa tsiku iye ankagwada pansi pa mawondo
ndipo amapemphera, kuyamika Mulungu wake, monga momwe ankachi-
tira kale. 11 Ndipo anthu awa anapita pamodzi ndi kukapeza Danieli
akupemphera ndi kupempha Mulungu wake kuti amuthandize. 12 Kotero
iwo anapita kwa mfumu ndipo anayankhula naye za lamulo lake kuti,
“Kodi simunasindikize lamulo lakuti pa masiku makumi atatu otsatirawa
aliyense amene apemphera kwa mulungu wina aliyense kapena kwa
munthu kupatula kwa inu mfumu, adzaponyedwa m'dzenje la mikango?”

Mfumu inayankha kuti, “Lamulo lilipobe monga mwa malamulo a
Amedi ndi Aperezi, amene sangathe kusinthika.”

13 Kenaka iwo anati kwa mfumu, “Danieli, amene ndi mmodzi mwa
akapolo ochokera ku Yuda, sakulabadira inu mfumu, kapena lamulo
limene munasindikizapo dzina lanu lija. Iye akupempherabe katatu pa
tsiku.” 14 Mfumu itamva izi, inavutika kwambiri mu mtima mwake.
Iyo inayesa kupeza njira yopulumutsira Danieli. Iyo inachita chotheka
chilichonse kufikira kulowa kwa dzuwa kuti imupulumutse.

15 Ndipo anthuwo anapita pamodzi kwa mfumu ndipo anati kwa
iye, “Kumbukirani, inu mfumu kuti monga mwa lamulo la Amedi
ndi Aperezi, palibe chimene mfumu inalamulira kapena kukhazikitsa
chimasinthidwa.”

16 Choncho mfumu inalamula, ndipo anabwera naye Danieli ndi
kukamuponya m'dzenje la mikango. Mfumu inati kwa Danieli, “Mulungu
wako amene umutumikira nthawi zonse, akupulumutse!”

17 Anatenga mwala natseka pa khoma pa dzenje la mikango, ndipo
mfumu inadindapo chizindikiro chake ndi cha nduna zake kuti wina

asasinthepo kanthu pa za Danieli. 18 Kenaka mfumu inabwerera ku
nyumba yake ndipo inakhala usiku wonse osadya kanthu, osalola chosan-
galatsa chilichonse. Ndipo sinagone tulo.
19 M'bandakucha, mfumu inanyamuka ndi kufulumira kupita ku dzenje
la mikango lija. 20 Itayandikira pa dzenjelo, inayitana Danieli moonetsa
nkhawa, "Danieli, mtumiki wa Mulungu wa moyo! Kodi Mulungu wako,
amene umutumikira nthawi zonse, wakulanditsa ku mikango?"
21 Danieli anayankha kuti, "Inu mfumu mukhale ndi moyo wautali!
22 Mulungu wanga anatumiza mngelo wake, ndipo anatseka pakamwa
pa mikango. Iyo sinandivulaze chifukwa Mulungu anaona kuti ndine
wosalakwa ndi kutinso sindinakulakwireni inu mfumu."
23 Mfumu inali ndi chimwemwe chopambana ndipo inalamulira kuti
amutulutse Danieli m'dzenjemo. Ndipo atamutulutsa Danieli m'dzenjemo,
sanapezeke ndi chilonda chilichonse pa thupi lake, chifukwa iye anadalira
Mulungu wake.
24 Mwa lamulo la mfumu, anthu onse amene ananeneza Danieli
aja anagwidwa ndi kukaponyedwa m'dzenje la mikango, pamodzi ndi
akazi awo ndi ana awo. Ndipo asanafike pansi pa dzenjelo, mikango
inawawakha ndi mphamvu ndi kuteketa mafupa awo onse.
25 Kenaka mfumu Dariyo inalembera anthu a mitundu yonse, ndi anthu
a ziyankhulo zosiyanasiyana a m'dziko lonse kuti,

"Mtendere uchuluke pakati panu!

26 "Ndikukhazikitsa lamulo kuti paliponse m'dziko langa anthu ayen-
era kuopa ndi kuchitira ulemu Mulungu wa Danieli.

"Popeza Iye ndi Mulungu wamoyo
ndi wamuyaya;
ufumu wake sudzawonongeka,
ulamuliro wake sudzatha.
27 Iye amalanditsa ndipo amapulumutsa,
amachita zizindikiro ndi zozizwitsa
kumwamba ndi pa dziko lapansi.
Iye walanditsa Danieli
ku mphamvu ya mikango."

28 Choncho Danieli anapeza ufulu pa nthawi ya ulamuliro wa Dariyo ndi
ulamuliro wa Koresi wa ku Perisiya.

# 7

*Maloto a Danieli a Zirombo Zinayi*

1 Chaka choyamba cha ufumu wa Belisazara wa ku Babuloni, Danieli
akugona pa bedi lake analota maloto ndipo anaona masomphenya. Iye
analemba malotowo mwachidule.
2 Danieli anati, "M'masomphenya anga usiku, ndinaona nyanga
yayikulu ikuvunduka ndi mphepo zochokera mbali zonse zinayi za
mlengalenga. 3 Ndipo m'nyangayo munatuluka zirombo zazikulu zinayi,
chilichonse chosiyana ndi chinzake.
4 "Choyamba chinali ngati mkango, ndipo chinali ndi mapiko ngati a chi-
wombankhanga. Ndinayang'anitsitsa, kenaka mapiko ake anakhadzuka
ndipo chinanyamulidwa ndi kuyimirira ndi miyendo yake iwiri ngati
munthu, ndipo anachipatsa mtima wa munthu.
5 "Ndipo ndinaona chirombo chachiwiri, chimene chimaoneka ngati
chimbalangondo. Chinali chonyamuka mbali imodzi, ndipo chinapana

nthiti zitatu m'kamwa mwake pakati pa mano ake. Anachilamula kuti, 'Nyamuka, idya nyama yambiri!'

6 "Pambuyo pake, ndinaona chirombo china, chimene chinkaoneka ngati kambuku. Pa msana pake chinali ndi mapiko anayi onga a mbalame. Chirombo ichi chinali ndi mitu inayi, ndipo chinapatsidwa mphamvu kuti chilamulire.

7 "Zitatha izi, m'masomphenya anga usiku, ndinaonanso chirombo chachinayi chitayima patsogolo panga. Chinali choopsa, chochititsa mantha ndi champhamvu kwambiri. Chinali ndi mano akuluakulu a chitsulo. Chimati chikatekedza ndi kumeza adani ake kenaka chinapondereza chilichonse chotsala. Ichi chinali chosiyana ndi zirombo zoyambirira zija, ndipo chinali ndi nyanga khumi.

8 "Ndikulingalira za nyangazo, ndinaona nyanga ina, yocheperapo, imene inkatuluka pakati pa zinzake. Zitatu mwa nyanga zoyamba zija zinazulidwa mwa icho. Nyanga iyi inali ndi maso a munthu ndi pakamwa pamene pankayankhula zodzitama.

9 "Ine ndikuyang'anabe ndinaona

"mipando yaufumu ikukhazikitsidwa,
ndipo Mkulu Wachikhalire anakhala pa mpando wake.
Zovala zake zinali zoyera ngati chisanu chowundana;
tsitsi la kumutu kwake linali loyera ngati thonje.
Mpando wake waufumu unali wonga malawi a moto,
ndipo mikombero yake yonse inkayaka moto.
10 Mtsinje wa moto unkayenda,
kuchokera patsogolo pake.
Anthu miyandamiyanda ankamutumikira;
ndipo anthu osawerengeka anayima pamaso pake.
Abwalo anakhala malo awo,
ndipo mabuku anatsekulidwa.

11 "Ndinapitiriza kuyang'anitsitsa chifukwa cha mawu odzitamandira amene nyanga ija inkayankhula. Ndili chiyang'anire choncho chirombo chachinayi chija chinaphedwa ndipo thupi lake linawonongedwa ndi
kuponyedwa m'ng'anjo ya moto. 12 Zirombo zina zija zinalandidwa
ulamuliro wawo, koma zinaloledwa kukhala ndi moyo kwa kanthawi.

13 "Ndikuyang'anabe zinthu m'masomphenya usiku, ndinaona wina ngati mwana wa munthu, akubwera ndi mitambo ya kumwamba. Anayandikira Mkulu Wachikhalire uja. Ena anamuperekeza kwa Iye.
14 Anapatsidwa ulamuliro, ulemerero ndi mphamvu za ufumu kuti anthu a mitundu ina yonse, mayiko ndi anthu aziyankhulo zosiyanasiyana apembedze iye. Mphamvu zake ndi mphamvu zamuyaya zimene sizidzatha, ndipo ufumu wake sudzawonongeka konse.

### *Tanthauzo la Maloto*

15 "Ine Danieli ndinavutika mu mzimu, ndipo zimene ndinaziona
m'masomphenya zinandisautsa m'maganizo. 16 Ndinayandikira mmodzi
mwa amene anayima pamenepo ndi kumufunsa tanthauzo lenileni la zonsezi.

"Kotero anandiwuza ndi kundipatsa tanthauzo la zinthu zonse izi:
17 'Zirombo zikuluzikulu zinayi zija ndi maufumu anayi amene adzaoneka
pa dziko lapansi. 18 Koma oyera mtima a Wammwambamwamba
adzalandira ufumu ndipo udzakhala nawo mpaka muyaya, inde ku nthawi zonse.'

[19] "Kenaka ndinafuna kudziwa tanthauzo lenileni la chirombo chachi-
nayi chija, chimene chinali chosiyana ndi zinzake zonse ndi choopsa
kwambiri, cha mano ake achitsulo ndi zikhadabo zamkuwa; chirombo
chimene chinapweteka ndi kumeza zinazo ndi kupondaponda chilichonse
chimene chinatsala. [20] Ndinafunanso kudziwa za nyanga khumi za pa
mutu pake ndiponso ina ija, nyanga imene inaphuka pambuyo pake
ndi kugwetsa zitatu zija. Imeneyi ndi nyanga ija yokhala ndi maso
ndi pakamwa poyankhula modzitamandira, ndipo inkaoneka yayikulu
kupambana zina zonse. [21] Ndikuyang'anitsitsa, nyanga imeneyi inathira
nkhondo anthu oyera mtima ndi kuwagonjetsa, [22] mpaka pamene
Mkulu Wachikhalire uja anafika ndi kuweruza mokomera oyera mtima
a Wammwambamwamba. Tsono nthawi inafika imene anthu oyera
mtimawo analandira ufumu.
[23] "Tsono anandifotokozera kuti, 'Chirombo chachinayi chija ndi ufumu
wachinayi umene udzaoneka pa dziko lapansi. Udzakhala wosiyana ndi
maufumu anzake onse ndipo udzawononga dziko lonse lapansi. Udza-
lipondaponda ndi kuliphwasula. [24] Nyanga khumi zija ndiwo mafumu
khumi amene adzatuluka mu ufumu umenewu. Pambuyo pake mfumu
ina idzadzuka, yosiyana ndi mafumu a m'mbuyomu; iyo idzagonjetsa
mafumu atatu. [25] Idzayankhula motsutsana ndi Wammwambamwamba
ndipo adzazunza oyera mtima ndi kusintha masiku azikondwerero ndi
malamulo. Oyera mtimawo adzalamulidwa ndi mfumuyi kwa zaka zitatu
ndi theka.
[26] " 'Koma bwalo lidzapereka chiweruzo, ndipo mphamvu zake zidza-
landidwa ndi kuwonongedwa kotheratu mpaka muyaya. [27] Kenaka
ulamuliro, mphamvu ndi ukulu wa maufumu pa dziko lonse lapansi
zidzaperekedwa kwa oyera mtima, a Wammwambamwamba. Ufumu
wawo udzakhala ufumu wosatha, ndipo olamulira onse adzawalamulira
ndi kuwamvera.' "
[28] "Apa ndiye pa mapeto pa nkhaniyi. Ine Danieli, ndinasautsidwa
kwambiri m'maganizo anga, ndipo nkhope yanga inasandulika, koma
ndinasunga nkhaniyi mu mtima mwanga."

# 8

## *Masomphenya a Danieli a Nkhosa Yayimuna ndi Mbuzi Yayimuna*

[1] Chaka chachitatu cha ulamuliro wa mfumu Belisazara, Ine Danieli,
ndinaonanso masomphenya, ena atatha amene anandionekera poyamba.
[2] Ndinaona m'masomphenya kuti ndinali mu mzinda wotetezedwa wa
Susa m'chigawo cha Elamu. M'masomphenyawo ndinaona nditayima pa-
fupi ndi mtsinje wa Ulai. [3] Nditakweza maso ndinaona nkhosa yayimuna
ya nyanga ziwiri, itayima pafupi ndi mtsinje. Nyanga zakezo zinali zazitali.
Nyanga imodzi inali yotalika kuposa inzake, ndipo iyi inaphuka inzakeyo
itamera kale. [4] Ndinaona nkhosa yayimunayo ikuthamanga mwaukali
kupita kumadzulo, kumpoto ndi kummwera. Palibe chirombo chimene
chikanatha kulimbana nayo, ndipo palibe akanatha kulanditsa kanthu
kwa iyo. Iyo inachita monga inafunira ndipo inali ndi mphamvu zambiri.
[5] Pamene ndinali kulingalira za zinthu zimenezi, mwadzidzidzi mbuzi
yayimuna inatulukira cha kumadzulo, kudutsa dziko lonse lapansi mwali-
wiro ikuyenda m'malele mokhamokha. Mbuzi yayimunayo inali ndi
nyanga yayikulu pakati pa maso ake. [6] Inabwera molunjika nkhosa
yayimuna ya nyanga ziwiri ija imene ndinaona itayima pafupi ndi mtsinje.

Ndipo inayithamangira mwaukali. 7 Inafika pafupi ndipo inalimbana nayo
mwaukali nkhosa yayimuna ija n'kuthyola nyanga zake ziwiri. Nkhosa
yayimunayo inalibenso mphamvu zogonjetsera mbuziyo; choncho mbuzi
ija inagwetsa nkhosayo pansi n'kuyipondaponda, ndipo palibe akanatha
kulanditsa nkhosayo kwa mbuziyo. 8 Mbuziyo inayamba kudzikuza
kwambiri chifukwa cha mphamvu zake koma pamene mphamvuzo
zinakula kwambiri nyanga yake yayikulu inathyoka, ndipo m'malo mwake
panamera nyanga zinayi moloza mbali zonse zinayi.

9 Pa imodzi mwa nyangazo panatuluka nyanga imene inali yochep-
erapo koma inakula kwambiri kuloza kummwera ndi kummawa ndi
kuloza dziko lokongola. 10 Inakula mpaka inafikira gulu lankhondo
la kumwamba, ndipo inagwetsera ena a gulu lankhondolo ndi ena a
gulu la nyenyezi ku dziko lapansi ndi kuwapondaponda. 11 Inadzikuza
yokha mpaka kufikira kwa mfumu ya gululo: inathetsa nsembe zimene
zinkaperekedwa tsiku ndi tsiku, ndipo inagwetsa nyumba yake yopatulika.
12 Gulu lake la nkhondo linathetsa nsembe zoperekera machimo za tsiku
ndi tsiku; chipembedzo choonadi chinaponderezedwa pansi. Nyangayi
inapambana mu zonse zimene inachita.

13 Kenaka ndinamva wina akuyankhula; ndipo woyera winanso ana-
mufunsa kuti, "Kodi zimene ndikuziona m'masomphenyazi zidzatha liti?
Nsembe zoperekera machimo za tsiku ndi tsiku zidzakhala zoletsedwa
mpaka liti? Nanga chonyansa chosokoneza chidzakhalapo mpaka liti?
Kodi gulu la ankhondo lidzapondereza malo opatulika mpaka liti?"

14 Iye anandiyankha kuti, "Zidzachitika patapita masiku 2,300; pambuyo
pake malo opatulika adzabwezeretsedwa monga kale."

### *Kumasulira kwa Masomphenya*

15 Ine Danieli ndikuyang'anitsitsa masomphenyawa ndi kuyesa
kuwazindikira, kuwamvetsa, ndinangoona wina wooneka ngati munthu
atayima patsogolo panga. 16 Ndipo ndinamva mawu a munthu kuchokera
m'mbali mwa mtsinje wa Ulai akuyitana kuti, "Gabrieli, muwuze
munthuyu tanthauzo la masomphenyawo."

17 Atayandikira kumene ndinayima, ndinachita mantha ndi kugwa
chafufumimba. Iye anati, "Mwana wa munthu, zindikira kuti masom-
phenyawa akunena za nthawi yachimaliziro."

18 Pamene ankandiyankhula ndinadzigwetsa pansi chafufumimba,
n'kugona tulo tofa nato. Kenaka anandikhudza ndi kundiyimiritsa.

19 Iye anati, "Ine ndikuwuza zimene zidzachitike ukadzatha mkwiyo,
chifukwa masomphenyawa ndi a nthawi ya chimaliziro." 20 Nkhosa
yayimuna ya nyanga ziwiri imene unayiona, ikuyimira mafumu a Amedi
ndi Aperezi. 21 Mbuzi yayimuna ija ndi mfumu ya Agriki, ndipo nyanga
yayikulu pakati pa maso ake aja ndi mfumu yoyamba. 22 Kunena za
nyanga inathyoka ija ndi nyanga zinayi zimene zinaphuka m'malo mwake
zikutanthauza maufumu anayi amene adzatuluka m'dziko lake; koma
sizidzafanana mphamvu ndi ufumu woyambawo.

23 "Pa masiku otsiriza a maufumuwa, machimo awo atachulukitsa,
padzadzuka mfumu yaukali ndi yochenjera kwambiri. 24 Idzakhala
yamphamvu kwambiri koma osati mphamvu za iyo yokha. Idzawononga
koopsa ndipo idzapambana mu chilichonse chimene idzachite. Mfumuyi
idzawononga anthu amphamvu ndi anthu oyera omwe. 25 Chifukwa cha
kuchenjera kwake chinyengo chidzachuluka pa nthawi ya ulamuliro wake,
ndipo idzadzikuza kuposa onse. Pamene oyera mtima adzaona ngati kuti

ali otetezedwa, iyo idzawononga ambiri ndi kuwukira ngakhale Mfumu ya
mafumu. Komabe idzawonongedwa, koma osati ndi mphamvu za munthu.
26 "Masomphenya okhudza madzulo ndi mmawa amene unawaona aja
ndi woona, koma uwasunge masomphenyawa mwachinsinsi popeza ndi
onena za masiku a m'tsogolo kwambiri."
27 Ine Danieli ndinafowoka ndipo ndinadwala masiku angapo. Kenaka
ndinadzuka ndi kupitiriza ntchito za mfumu. Ndinada nkhawa ndi
masomphenyawo; ndipo sindinathe kuwamvetsa.

# 9

*Pemphero la Danieli*

1 M'chaka choyamba cha Dariyo mwana wa Ahasiwero (wochokera
kwa Amedi), amene anakhala mfumu ya ku Babuloni, 2 ine Danieli
ndinazindikira powerenga mawu a Yehova opatsidwa kwa mneneri
Yeremiya, kuti Yerusalemu adzakhala bwinja kwa zaka 70. 3 Choncho
ndinatembenukira kwa Ambuye Mulungu ndipo ndinamudandaulira ndi
kupempha posala kudya, ndi kuvala chiguduli ndi kudzola phulusa.
4 Ndinapemphera kwa Yehova Mulungu wanga ndi kuvomereza kuti
tinachimwa:

Ndinati, "Inu Ambuye, Mulungu wamkulu ndi woopsa, amene muma-
sunga pangano lanu la chikondi kwa onse amene amakukondani ndi
kumvera malamulo anu, 5 tachimwa ndipo tachita zolakwa ndi zoyipa.
Takuwukirani posiya malangizo ndi malamulo anu. 6 Sitinamvere
aneneri atumiki anu, amene anayankhula m'dzina lanu kwa mafumu
athu, kwa akalonga athu, makolo athu, ndi kwa anthu onse a m'dziko.
7 "Ambuye ndinu olungama, koma lero tili ndi manyazi, ife anthu a ku
Yuda, a ku Yerusalemu ndi Israeli yense, apafupi ndi akutali omwe, ku
mayiko onse kumene munatipirikitsira chifukwa cha kusakhulupirika
kwathu. 8 Inu Yehova, ife ndi mafumu athu, akalonga athu ndi
makolo athu tili ndi manyazi chifukwa takuchimwirani. 9 Ambuye
Mulungu wathu ndi wachifundo ndi wokhululuka, ngakhale kuti
tamuwukira: 10 Ife sitinamvere Yehova Mulungu wathu kapena kusunga
malamulo ake amene anatipatsa kudzera mwa aneneri atumiki ake.
11 Aisraeli onse anachimwira lamulo lanu motero anapatuka, nakana
kukumverani.

"Choncho matemberero ndi olumbira amene alembedwa m'malamulo
a Mose, mtumiki wa Mulungu, atigwera chifukwa takuchimwirani.
12 Inu mwakwaniritsa mawu amene munayankhula otitsutsa ife ndi
otsutsa otilamulira potibweretsera tsoka lalikulu. Pa dziko lapansi
sipanachitikenso zinthu ngati zimene zaonekera Yerusalemu. 13 Monga
kunalembedwa m'Malamulo a Mose, tsoka lililonse latifikira chikhalire-
cho sitinapemphe Yehova Mulungu wathu kuti atikomere mtima. Siti-
nasiye machimo athu, ndipo sitinasamale choonadi chanu. 14 Choncho
Yehova anakonza kuti atigwetsere tsoka limeneli, ndipo wachitadi
popeza Yehova Mulungu wathu ndi wolungama mu chilichonse ama-
chita; chikhalirecho ife sitinamumvere.
15 "Inu Ambuye Mulungu wathu, munatulutsa anthu anu ku Igupto ndi
dzanja lanu lamphamvu ndipo dzina lanu ndi lotchuka mpaka lero. Ife
tachimwa, tachita zolakwa. 16 Inu Ambuye, molingana ndi zochita zanu
zolungama, tikukupemphani kuti muchotse mkwiyo ndi ukali wanu

pa Yerusalemu mzinda wanu, phiri lanu loyera. Machimo athu ndi mphulupulu za makolo athu zachititsa kuti onse otizungulira atonze Yerusalemu ndi anthu anu.
17 "Tsopano Mulungu wathu, imvani mapemphero ndi zopempha za mtumiki wanu. Kuti anthu onse akudziweni kuti ndinu Ambuye, komerani mtima malo anu opatulika amene asanduka bwinja.
18 Tcherani khutu, Inu Mulungu, ndipo imvani; tsekulani maso anu ndipo onani mabwinja athu ndi mzinda umene umadziwika ndi dzina lanu. Sitikupempha chifukwa chakuti ndife olungama, koma chifukwa
cha kukula kwa chifundo chanu. 19 Inu Ambuye imvani mawu
athu! Ambuye khululukani! Ambuye timvereni, ndipo muchitepo kanthu! Kuti anthu adziwe kuti Inu ndinu Mulungu wanga musachedwe chifukwa mzinda wanu ndi anthu anu amadziwika ndi dzina lanu."

### *Zaka 70*

20 Ndikuyankhula ndi kupemphera, kuvomereza machimo anga ndi machimo a anthu anga Aisraeli ndi kupempherera phiri lake loyera
kwa Yehova Mulungu wanga, 21 Gabrieli, munthu uja amene ndinamuona m'masomphenya poyambirira, anabwera kwa ine mowuluka. Iyi
inali nthawi ya nsembe ya madzulo. 22 Anandilangiza kuti, "Danieli ndabwera tsopano kuti ndikupatse nzeru kuti uzitha kumvetsa zinthu.
23 Utangoyamba kupemphera, Mulungu anayankha. Tsono ine ndabwera kudzakuwuza yankholo, popeza ndiwe wokondedwa kwambiri. Choncho mvetsetsa pamene ndikufotokoza za zinthu zimene unaziona m'masomphenya.

24 "Zaka 490 zinayikidwa kuti anthu a mtundu wako ndi mzinda wanu woyera aleke zoyipa, asiye tchimo. Iwo adzapereka dipo kupepesera zolakwa zawo. Zikadzatero anthu adzaonetsa moyo wachilungamo nthawi zonse. Izi zidzatsimikiza zimene unaziona m'masomphenya zija ndi zimene ananenera aneneri. Malo opatulika adzakhazikitsidwa.

25 "Tsono udziwe ndipo uzindikire izi kuti kuyambira pamene lamulo linaperekedwa kuti Yerusalemu akonzedwenso mpaka pamene mfumu Yodzozedwa idzafike padzapita zaka 49. Pa zaka 434 mzinda wa Yerusalemu udzamangidwanso, ndipo mabwalo ndi ngalande zake zidzatetezedwa. Koma nthawiyi idzakhala ya masautso. 26 Patatha zaka
434, Wodzozedwayo adzaphedwa ndipo sadzakhala ndi aliyense. Anthu a wolamulira amene adzabwere adzawononga mzinda ndi Nyumba ya Mulungu. Kutha kwake kudzafika ngati chigumula. Komabe nkhondo idzapitirira mpaka chiwonongeko chimene Mulungu ananeneratu chitachitika. 27 Adzachita pangano lolimba ndi anthu ambiri kwa zaka
zisanu ndi ziwiri. Koma pakatin'pakati pa sabata limodzilo iye adzaletsa kupereka nsembe ndi chopereka. Chonyansa chosakaza chija adzachiyika m'Nyumba ya Mulungu, ndipo chidzakhalapobe mpaka wochita zimenezi atalangidwa ndi chiwonongeko chimene Mulungu ananeneratu."

## 10

### *Masomphenya a Danieli a Munthu*

1 Chaka chachitatu cha Koresi mfumu ya Aperezi, Danieli amene ankatchedwa Belitesezara analandira mawu a vumbulutso. Uthenga wake unali woona ndipo anawumvetsa movutikira. Uthengawu anawumva kudzera m'masomphenya.

[2] Pa nthawi imeneyi, ine Danieli ndinalira kwa masabata atatu.
[3] Sindinadye chakudya chokoma; nyama ndi vinyo sizinakhudze milomo
yanga ndi pang'ono pomwe; ndipo sindinadzole mafuta aliwonse mpaka
patatha masabata atatu.

[4] Pa tsiku la 24 la mwezi woyamba, nditayima m'mbali mwa mtsinje
waukulu wa Tigirisi, [5] ndinakweza maso ndipo ndinaona kuti pafupi ndi
ine panali munthu wochokera ku Ufazi atavala zovala zosalala ndi lamba
wa golide woyengeka bwino m'chiwuno mwake. [6] Thupi lake linali ngati
mwala wonyezimira, nkhope yake ngati chiphaliwali, maso ake ngati muni
wowala, manja ndi miyendo yake ngati mkuwa wowala, ndipo mawu ake
ngati liwu la chikhamu cha anthu.

[7] Ine Danieli ndinali ndekha pamene ndinaona masomphenyawa; anthu
amene anali ndi ine sanawaone, koma anadzazidwa ndi mantha kotero
kuti anathawa ndi kukabisala. [8] Choncho ndinatsala ndekha, ndikuonet-
setsa masomphenya a ulemererowa. Ndiye nkhope yanga inasinthika,
ndinalefuka, ndipo ndinalibenso mphamvu. [9] Kenaka ndinamva iye
akuyankhula, ndipo pamene ndinkamvetsera, ndinagwa chafufumimba
ndi kugona tulo tofa nato.

[10] Dzanja linandikhudza ndi kundinyamula ndipo ndinachita ngati
kuwerama pa mawondo manja atagwira pansi. [11] Iye anati, "Danieli,
iwe wokondedwa kwambiri, imirira ndipo uganizire mosamala mawu
ndiyankhule kwa iwe, popeza tsopano ndatumidwa kwa iwe." Atanena
izi kwa ine ndinayimirira monjenjemera.

[12] Ndipo iye anapitiriza nati, "Usachite mantha Danieli. Kuyambira
tsiku loyamba pamene unatsimikiza mtima kuti umvetse zinthuzi ndi
kudzichepetsa pamaso pa Mulungu wako, pempho lako linamveka ndipo
ndabwera kudzayankha mapemphero akowo. [13] Koma mtsogoleri wa
ufumu wa Peresiya ananditchingira pa masiku 21, kenaka Mikayeli,
mmodzi mwa angelo akuluakulu anadza kudzandithandiza chifukwa
ndinakhala komweko ndi mafumu a ku Peresiya. [14] Tsopano ndafika
kuti ndidzakufotokozere zimene zidzachitika kwa anthu a mtundu wako
kutsogolo. Ndipo pali masomphenya enanso okhudza nthawi imene
ikudza."

[15] Pa nthawi yomwe ankanena izi kwa ine, ndinazolika nkhope yanga
pansi kusowa chonena. [16] Kenaka wina wa maonekedwe ngati munthu
anakhudza milomo yanga, ndipo ndinatsekula pakamwa panga ndi
kuyamba kuyankhula. Ndinati kwa amene anayima patsogolo panga, "Ine
ndasweka mtima chifukwa cha masomphenyawa mbuye wanga, ndipo
ndalefuka. [17] Kodi ine mtumiki wamba wa mbuye wanga ndingathe
bwanji kuyankhula ndi inu mbuye wanga? Mphamvu zanga zatha, ndipo
ndikulephera kupuma."

[18] Kenaka wooneka ngati munthu uja anandikhudzanso ndipo anandi-
patsa mphamvu. [19] Iye anati, "Usachite mantha, munthu wokondedwa
kwambiriwe. Mtendere ukhale ndi Iwe ndipo ukhale wolimba."

Atayankhula nane, ndinalimbikitsidwa ndipo ndinati, "Yankhulani
Mbuye wanga, popeza mwandipatsa mphamvu."

[20] Ndipo iye anati, "Kodi ukudziwa chifukwa chimene ndabwerera kwa
iwe? Ndiyamba ndabwerera kukamenyana ndi mtsogoleri wa ufumu wa
Peresiya, ndipo ndikakanthana naye, kenaka mtsogoleri wa ufumu wa
Grisi adzabwera. [21] Koma ndikuwuza zimene zalembedwa m'buku la

zoona koma palibe wondithandiza kulimbana nawo kupatula Mikayeli, kalonga wako.”

# 11

1 Ndipo chaka choyamba cha Dariyo Mmedi ine Mikayeli ndinabwera kumuthandiza ndi kumuteteza Gabrieli.

### *Mafumu a Kummwera ndi Kumpoto*

2 “Ndipo tsopano ndikuwuza zoona: Mafumu ena atatu adzalamulira ku Peresiya, ndipo kenaka padzadzuka mfumu yachinayi imene idzakhala yolemera kwambiri kuposa onsewo. Popeza kuti idzakhala ndi mphamvu chifukwa cha chuma chake, idzadzutsa onse kuti alimbane ndi ufumu wa Grisi.
3 Kenaka mfumu yamphamvu idzafika imene idzalamulira ndi ufumu waukulu ndi kuchita zimene ifuna.
4 Koma ufumu wake ukadzafika pachimake, udzawonongedwa ndi kugawidwa m’zigawo zinayi. Ufumuwo sudzaperekedwa kwa zidzukulu zake, ndipo olowa m’malo mwake sadzakhala ndi mphamvu monga anali nazo, chifukwa ufumu wake udzazulidwa ndi kuperekedwa kwa ena.
5 “Mfumu ya kummwera idzakhala yamphamvu, koma mmodzi mwa akalonga ake adzakhala ndi mphamvu kuposa iyo; adzalamulira ufumu wake waukulu kwambiri.
6 Patapita zaka zingapo, mfumu ya kummwera ndi mfumu ya kumpoto adzachita pangano. Mwana wamkazi wa mfumu ya kummwera adzapita nakakwatiwa ndi mfumu ya kumpoto pokhazikitsa pangano la mtendere, koma ulamuliro wake pamodzi ndi wa mwana wake sudzakhalitsa. M’masiku amenewo iye, mwamuna wake, mwana wake ndi atumiki ake, onse adzaperekedwa kwa adani.
7 “Mmodzi wochokera ku banja la mkaziyo adzadzuka nadzalamulira m’malo mwake. Iye adzamenyana ndi ankhondo a mfumu ya kumpoto ndi kulowa m’malo ake otetezedwa; adzachita nawo nkhondo ndi kupambana.
8 Iye adzalandanso milungu yawo, mafano awo achitsulo, ndi ziwiya zawo zamtengowapatali zasiliva ndi golide ndi kubwerera nazo ku Igupto. Adzaleka osayithira nkhondo mfumu ya kumpoto kwa zaka zingapo.
9 Kenaka mfumu ya kumpoto idzathira nkhondo dziko la mfumu ya kummwera koma idzalephera ndi kubwerera kwawo.
10 Ana ake adzakonzekera nkhondo ndi kusonkhanitsa gulu lankhondo lalikulu, limene lidzathira nkhondo mfumu yakummwera ngati chigumula mpaka kumalo ake otetezedwa.
11 “Kenaka mfumu yakummwera idzatuluka mokwiya ndi kumenya nkhondo ndi mfumu yakumpoto, imene idzasonkhanitsa gulu lalikulu la nkhondo, koma idzayigonjetsa.
12 Gulu la nkhondoli likadzagwidwa, mfumu yakummwera idzayamba kudzikuza ndipo idzapha anthu miyandamiyanda, koma kupambanaku sikudzapitirira.
13 Popeza mfumu ya kumpoto idzasonkhanitsa gulu lina lankhondo, lochulukirapo kuposa loyamba; ndipo patapita zaka zingapo idzabwera ndi chigulu chachikulu cha nkhondo chokonzekeratu ndi zida.
14 “Nthawi imeneyo ambiri adzawukira mfumu ya kummwera. Anthu achisokonezo pakati panu nawonso adzawukira pokwaniritsa masomphenya, koma sadzapambana.
15 Kenaka mfumu ya kumpoto idzafika ndikuzinga mzinda powunda nthumbira za nkhondo ndipo idzagonjetsa mzinda wotetezedwa. Gulu lankhondo la kummwera lidzasowa mphamvu; ngakhale akatswiri awo ankhondo sadzakhala ndi mphamvu zogonjetsera ankhondo a kumpoto.
16 Mfumu ya kumpoto

idzachita zofuna zake; palibe aliyense adzayigonjetse. Idzakhazikitsa
ulamuliro wake mu Dziko Lokongola. Zonse zidzakhala mu ulamuliro
wa mfumu yakumpoto ija. 17 Idzafika ndi mphamvu za ufumu wake
wonse ndipo idzayesa kuchita pangano la mtendere ndi mfumu ya
kummwera. Ndipo idzamupatsa mwana wake wamkazi kuti amukwatire
ndi cholinga cholanda ufumu, koma zolinga zake sizidzatheka kapena
kumuthandiza. 18 Kenaka idzatembenukira ku mayiko a m'mbali mwa
nyanja ndi kulanda mizinda yambiri, koma mtsogoleri wina wa nkhondo
adzathetsa kudzikuza kwakeko ndipo adzabwezera chipongwecho kwa
iye. 19 Zikadzatha izi, mfumu idzabwerera ku malo otetezedwa a dziko
la kwawo koma idzapunthwa ndi kugwa osapezekanso.

20 "Mfumu imene idzatenga malo ake idzatumiza wokhometsa msonkho
kuti chuma cha ufumu wake chichuluke. Komabe m'zaka zochepa
mfumuyo idzawonongedwa osati mu mkwiyo kapena ku nkhondo.

21 "M'malo mwake mudzalowa munthu wonyozeka amene si wa banja
laufumu. Iye adzabwera pamene anthu akuganiza kuti ali pa mtendere,
ndipo adzalanda ufumuwo mwa chinyengo. 22 Kenaka adzagonetsa
gulu lalikulu lankhondo kuphatikizapo Mkulu wa Ansembe wapangano.
23 Atatha kuchita naye pangano, iye adzachita monyenga, ndipo ngakhale
adzakhale ndi anthu ochepa adzakhalabe ndi mphamvu. 24 Mwadzidzidzi,
iye adzazithira nkhondo zigawo zolemera kwambiri ndipo adzachita
zimene makolo ake ngakhale agogo ake sanachitepo. Iye adzagawira
zolanda, zofunkha ndi chuma kwa omutsatira. Adzachita chiwembu
cholanda mizinda yotetezedwa koma kwa kanthawi kochepa.

25 "Mfumu ya kumpoto idzalimba mtima, ndipo idzasonkhanitsa gulu
lalikulu la ankhondo kuti lithire nkhondo mfumu yakummwera. Mfumu
yakummwera ndi gulu lake lankhondo lalikulu ndi lamphamvu idza-
thirana nkhondo ndi mfumu yakumpoto koma sidzapambana chifukwa
cha ziwembu zimene adzamukonzera. 26 Amene amadya chakudya
ndi mfumu adzamuukira; gulu lake lankhondo lidzagonjetsedwa, ndipo
ambiri adzafera ku nkhondo. 27 Mafumu awiriwa mitima yawo idzalinga
ku zoyipa. Azidzanamizana ali pa tebulo limodzi, koma zolinga zawo
sizidzatheka chifukwa nthawi idzakhala isanakwane. 28 Mfumu ya
kumpoto idzabwerera ku dziko la kwawo ndi chuma chambiri, koma
mtima wake udzafunitsitsa pangano lopatulika. Idzawononga panganolo
ndipo kenaka idzabwerera ku dziko lake.

29 "Patapita nthawi mfumu ya kumpoto idzabwereranso kummwera
koma sidzapambana monga inachitira kale. 30 Sitima zapamadzi zo-
chokera ku mayiko a ku madzulo zidzalimbana naye, ndipo adzataya
mtima. Kenaka idzabwerera mopsa mtima ndi kudzalimbana ndi
chipembedzo cha anthu opatulika. Idzabwerera ndi kuchitira chifundo
amene sadzasunga pangano loyera.

31 "Ankhondo ake adzayipitsa linga la Nyumba ya Mulungu ndipo
adzathetsa nsembe za tsiku ndi tsiku. Kenaka adzakhazikitsa chonyansa
chimene chabweretsa chiwonongeko. 32 Ndi mawu oshashalika mfumuyo
idzakopa amene anaphwanya pangano, koma anthu amene amadziwa
Mulungu wawo adzalimbika ndipo adzayikana mfumuyo kwathunthu.

33 "Amene ndi anzeru adzalangiza ambiri. Koma patapita kanthawi
adzaphedwa ndi lupanga kapena kutenthedwa, kapena kugwidwa kapena
kulandidwa katundu. 34 Pa nthawi yozunzikayi ena adzawathandiza
pang'ono, koma ambiri othandizawo adzakhala achinyengo. 35 Ena mwa

anzeruwo adzaphedwa ndi cholinga chakuti ayengedwe, otsala mwa iwo ayeretsedwe ndi kukhala wopanda banga kufikira nthawi yomaliza, popeza idzafika ndithu nthawi imene Mulungu wayika.

*Mfumu Yodzikweza*

36 "Mfumu ya kumpoto idzachita zimene ikufuna. Idzadzikweza ndi kudziyesa yopambana mulungu aliyense ndipo idzanenera za mwano Mulungu wa milungu. Iyo idzapambana mpaka nthawi yoti Mulungu ayilange mwa mkwiyo itakwana popeza chimene chatsimikizika chiyenera
kuchitika. 37 Mfumuyo idzanyoza milungu ya makolo ake ndiponso mulungu wokondedwa ndi akazi, sidzachitiranso ulemu mulungu aliyense,
koma idzadzikweza yokha pamwamba pa onse. 38 M'malo mwa onsewo, idzachitira ulemu mulungu wachitetezo; mulungu wosadziwika ndi makolo ake. Iyo idzapereka kwa mulunguyo golide ndi siliva, ndi miyala yokongola, ndiponso mphatso za pamwamba kwambiri.
39 Anthu opembedza mulungu wachilendo adzakhala ngati linga lake. Idzalemekeza iwowa kwambiri, ndipo idzawayika kuti alamulire anthu ambiri. Idzawagawira dziko ngati malipiro awo.
40 "Pa nthawi yomaliza mfumu yakummwera idzachita nkhondo ndi mfumu yakumpoto. Koma mfumu yakumpotoyi idzayikantha ndi magaleta ndi akavalo ndi sitima zapamadzi zambiri ngati mphepo yamkokomo. Idzalowa m'mayiko ambiri ndikuwakokolola onse ngati
madzi osefukira. 41 Idzalowanso m'Dziko Lokongola ndipo anthu ambiri adzaphedwa. Koma Edomu, Mowabu ndi olamulira a Amoni adzapu-
lumuka. 42 Idzathira nkhondo mayiko ambiri ndipo ngakhale Igupto
sadzapulumuka. 43 Idzalanda chuma cha golide, siliva, ndi zonse za mtengowapatali za ku Igupto, ndiponso anthu a ku Libiya ndi Akusi
adzagonja kwa iwo. 44 Koma uthenga wochokera kummawa ndi kumpoto udzayiopsa, ndipo idzapita ndi ukali kukawononga ndi kutheratu anthu
ambiri. 45 Mfumuyo idzayimika matenti ake aufumu, pakati pa nyanja ndi phiri lokongola. Komabe mapeto ake mfumuyo idzaphedwa, ndipo palibe amene adzayithandize."

# 12

*Nthawi Yotsiriza*

1 "Pa nthawi imeneyo Mikayeli, mngelo wamkulu amene amateteza anthu a mtundu wako, adzabwera. Imeneyi idzakhala nthawi ya mavuto aakulu omwe sanaonekepo kuyambira pachiyambi cha mitundu ya anthu mpaka nthawi ikudzayo. Komatu pa nthawiyi anthu a mtundu wako, aliyense amene dzina lake lidzapezeke lolembedwa m'buku adzapulu-
mutsidwa. 2 Ambiri mwa amene akugona m'nthaka adzadzuka: ena adzapita ku moyo wosatha, ena ku malo amanyazi ndi chilango chosatha.
3 Amene ali anzeru m'njira ya chilungamo adzawala ngati kuwala kwa mlengalenga, ndipo amene alondolera ambiri ku njira yolungama,
adzawala ngati nyenyezi ku nthawi zosatha. 4 Koma iweyo, Danieli, sungitsa mawuwa, umate bukuli kufikira nthawi ya chimaliziro. Anthu ambiri adzapita uku ndi uko ndipo nzeru zidzanka zikukulirakulira."

5 Kenaka ine Danieli poyang'ana ndinaona anthu ena awiri atayima,
wina tsidya lino la mtsinje, wina tsidya linalo. 6 Mmodzi mwa awiriwo anafunsa munthu wovala chovala chosalala amene anali m'mbali mwa

madzi a mu mtsinje uja kuti, “Kodi padzapita nthawi yayitali bwanji kuti zodabwitsazi zidzakwaniritsidwe?”

7 Munthu wovala chovala chosalala, amene anali m’mbali mwa madzi a mu mtsinje uja, anakweza dzanja lake lamanja ndi lamanzere kumwamba, ndipo ndinamumva akulumbira m’dzina la Wamoyo ku nthawi zonse uja kuti, “Zidzachitika patapita zaka zitatu ndi theka. Zinthu zonsezi zidzachitika akadzatha masautso amene agwera anthu olungama.”

8 Ndinamva, koma sindinamvetsetse. Choncho ndinafunsa kuti, “Mbuye wanga, nanga matsiriziro a zonsezi adzakhala chiyani?”

9 Ndipo anandiyankha kuti, “Pita iwe Danieli, pakuti mawuwa ndi osungidwa ndi omatidwa kufikira nthawi ya chimaliziro.
10 Anthu ambiri adzayeretsedwa nakhala olungama wopanda chodetsa, koma oyipa adzakhala chiyipire. Palibe mmodzi wa anthu oyipa amene adzamvetsetsa koma okhawo amene ali anzeru adzamvetsetsa.

11 “Kuyambira pamene nsembe ya tsiku ndi tsiku idzathetsedwa ndi kukhazikitsa kwa chonyansa chobweretsa chisokonezo chija, padzapita masiku 1,290.
12 Wodala munthu amene adikirabe nadzafika pa mapeto a masiku 1,335.

13 “Koma iweyo Danieli, pitiriza ndipo ulimbikire mpaka matsiriziro. Kenaka udzamwalira. Koma m’masiku otsiriza udzauka kuti ulandire gawo lako.”

# Hoseya

1 Awa ndi mawu amene Yehova anayankhula kwa Hoseya mwana wa
Beeri pa nthawi ya ulamuliro wa Uziya, Yotamu, Ahazi ndi Hezekiya,
mafumu a ku Yuda ndiponso pa nthawi ya ulamuliro wa Yeroboamu
mwana wa Yowasi mfumu ya ku Israeli.

*Mkazi wa Hoseya ndi Ana Ake*

2 Yehova atayamba kuyankhula kudzera mwa Hoseya, Yehova anati kwa
Hoseyayo, "Pita kakwatire mkazi wachiwerewere ndipo ubereke naye ana
m'chiwerewere chake pakuti anthu a m'dziko muno achimwa pochita
chigololo choyipitsitsa, posiya Yehova." 3 Motero Hoseya anakwatira
Gomeri mwana wamkazi wa Dibulaimu, ndipo mkaziyo anakhala woyem-
bekezera nabala mwana wamwamuna.
4 Tsono Yehova anati kwa Hoseya, "Umutche dzina loti Yezireeli, pakuti
ndili pafupi kulanga banja la Yehu chifukwa cha anthu amene anawapha
ku Yezireeli ndipo ndidzathetsa ufumu wa Israeli. 5 Tsiku limenelo
ndidzathyola uta wa Israeli m'chigwa cha Yezireeli."
6 Gomeri anakhala woyembekezeranso ndipo anabereka mwana
wamkazi. Ndipo Yehova anati kwa Hoseya, "Umutche dzina loti 'Sakond-
edwa' pakuti sindidzaonetsanso chikondi changa pa nyumba ya Israeli,
kuti ndingawakhululukire konse. 7 Komatu ndidzaonetsa chikondi pa
nyumba ya Yuda; ndipo ndidzawapulumutsa, osati ndi uta, lupanga
kapena nkhondo, kapena akavalo ndi okwerapo ake, koma ine Yehova
Mulungu wawo ndidzawapulumutsa."
8 Sakondedwa ataleka kuyamwa, Gomeri anabereka mwana wina
wamwamuna. 9 Pamenepo Yehova anati, "Umutche dzina loti
Sianthuanga," pakuti inu si ndinu anthu anga ndipo Ine si ndine Mulungu
wanu.
10 "Komabe Aisraeli adzachuluka ngati mchenga wa m'mbali mwa
nyanja umene sangathe kuwuyeza kapena kuwuwerenga. Pamalo omwe
ananena kuti, 'Sindinu anthu anga,' pomweponso adzawatchula kuti
'Ana a Mulungu wamoyo.' 11 Anthu a ku Yuda ndi anthu a ku
Israeli adzasonkhananso pamodzi ndipo adzasankha mtsogoleri mmodzi
ndi kutuluka m'dzikomo, pakuti tsiku la Yezireeli lidzakhala lalikulu
kwambiri."

## 2

1 "Nena kwa abale ako kuti, 'Ndinu anthu anga,' kwa alongo ako kuti
'Ndinu okondedwa anga.' "

*Kulangidwa ndi Kubwezeretsedwa kwa Israeli*

2 "Dzudzulani amayi anu, adzudzuleni iwo,
pakuti si mkazi wanga,
ndipo ine sindine mwamuna wake.
Iyeyo achotse maonekedwe adama pa nkhope yake,
ndi kusakhulupirika pa mawere ake.
3 Akapanda kutero ndidzamuvula,
ndipo adzakhala wamaliseche monga tsiku limene anabadwa;
ndidzamuwumitsa ngati chipululu,
adzakhala ngati dziko lopanda madzi,

ndi kumupha ndi ludzu.
4 Sindidzaonetsa chikondi changa pa ana ake,
chifukwa ndi ana a m'chiwerewere.
5 Amayi awo akhala akuchita zachiwerewere
ndipo anawabereka anawo akuchita zinthu zochititsa manyazi.
Iwo anati, 'Ine ndidzatsatira zibwenzi zanga,
zimene zimandipatsa chakudya ndi madzi,
ubweya ndi thonje, mafuta ndi chakumwa.'
6 Choncho njira yake ndidzayitseka ndi minga;
ndidzamuzinga ndi khoma kotero kuti sadzapezanso njira yotulukira.
7 Adzathamangira zibwenzi zake koma sadzazipeza;
adzazifunafuna koma sadzazipeza.
Pamenepo iye adzati,
'Ndibwerera kwa mwamuna wanga woyamba uja,
pakuti ndinali pabwino ndi iyeyo kusiyanitsa ndi pano.'
8 Iye sanazindikire kuti ndine amene
ndinkamupatsa tirigu, vinyo watsopano ndi mafuta.
Ndine amene ndinkamukhuthulira siliva ndi golide,
zimene ankapangira mafano a Baala.

9 "Choncho Ine ndidzamulanda tirigu wanga pa nthawi yokolola,
ndi vinyo wanga watsopano pa nthawi yopsinya mphesa.
Ndidzamulanda ubweya ndi thonje langa,
zomwe akanaphimba nazo umaliseche wake.
10 Motero tsopano ndidzaonetsa maliseche ake
pamaso pa zibwenzi zake;
palibe ndi mmodzi yemwe adzamupulumutse m'manja mwanga.
11 Ndidzathetsa zikondwerero zake zonse:
zikondwerero zake za chaka ndi chaka, za mwezi watsopano,
za pa masiku a Sabata ndi maphwando ake onse a pa masiku okhazikitsidwa.
12 Ndidzawononga mitengo yake ya mpesa ndi mitengo yake yamkuyu,
imene iye ankanena kuti inali malipiro ake ochokera kwa zibwenzi zake.
Ndidzayisandutsa chithukuluzi,
ndipo zirombo zakuthengo zidzadya zipatsozo.
13 Ndidzamulanga chifukwa cha masiku
amene anafukiza lubani kwa Abaala;
anadzikongoletsa povala mphete ndi mikanda yamtengowapatali
ndipo anathamangira zibwenzi zake,
koma Ine anandiyiwala,"
akutero Yehova.

14 "Koma tsopano ndidzamukopa mkaziyo;
ndidzapita naye ku chipululu
ndipo ndidzamuyankhula mwachikondi.
15 Kumeneko ndidzamubwezera minda yake ya mpesa,
ndipo ndidzasandutsa Chigwa cha Akori kukhala khomo la chiyembekezo.
Kumeneko iye adzayimba nyimbo monga m'masiku a ubwana wake,
monga tsiku limene anatuluka ku Igupto.

16 “Tsiku limeneli,” Yehova akuti,
“udzandiyitana kuti, ‘Amuna anga;’
sudzandiyitananso kuti, ‘Mbuye wanga.’
17 Ndidzachotsa mayina a Abaala pakamwa pake;
sadzatchulanso mayina awo popemphera.
18 Tsiku limenelo ndidzachita pangano
ndi zirombo zakuthengo ndi mbalame zamumlengalenga
ndiponso zolengedwa zokwawa pansi kuti ziyanjane ndi anthu anga.
Ndidzachotsa m’dzikomo uta,
lupanga ndi zida zonse zankhondo,
kuti onse apumule mwamtendere.
19 Ndidzakutomera kuti ukhale mkazi wanga mpaka muyaya;
ndidzakutomera mwachilungamo, mwaungwiro,
mwachikondi ndi mwachifundo.
20 Ndidzakutomera mokhulupirika
ndipo udzadziwa Yehova.

21 “Tsiku limenelo Ine ndidzayankha,”
akutero Yehova.
“Ndidzayankha mlengalenga pempho lake lofuna mitambo
ndipo mvula idzagwa pa dziko lapansi;
22 ndipo nthaka idzamvera kupempha kwa tirigu,
vinyo ndi mafuta,
ndipo zidzamvera Yezireeli.
23 Ndidzadzala Israeli m’dziko kuti akhale wanga:
ndidzaonetsa chikondi changa kwa anthu amene ndinkawatchula dzina loti, ‘Sakondedwa.’
Ndidzawawuza amene ndinkawatchula dzina loti, ‘Si anthu anga,’ kuti, ‘Ndinu anthu wanga;’
ndipo adzanena kuti, ‘ndinu Mulungu wathu,’ ”

# 3

*Hoseya Ayanjana ndi Mkazi Wake*

1 Yehova anati kwa ine, “Pita kamukondenso mkazi wako, ngakhale
ali pa chibwenzi ndi wina ndi kuti ndi wachigololo. Mukonde iyeyo
monga momwe Yehova amakondera Aisraeli, ngakhale iwo amapita
kukapembedza milungu ina ndi kukonda nsembe za keke zamphesa
zowuma.”
2 Motero ndinamukwatira popereka ndalama khumi ndi zisanu zasiliva,
ndiponso mitanga isanu ndi iwiri ya barele.
3 Kenaka ndinamuwuza
mkaziyo kuti, “Ukhale nane masiku ambiri; usachitenso zachiwerewere
kapena chigololo ndi munthu wina, ndipo ine ndidzakhala nawe.”
4 Pakuti Aisraeli adzakhala masiku ambiri opanda mfumu kapena
kalonga, osapereka nsembe kapena kuyimika miyala yachipembedzo,
wopanda efodi kapena fano.
5 Pambuyo pake Aisraeli adzabwerera ndi
kufunafuna Yehova Mulungu wawo ndi Davide mfumu yawo. Adzabwera
kwa Yehova akunjenjemera ndipo adzalandira madalitso m’masiku awo
otsiriza.

# 4

*Yehova Ayimba Mlandu Israeli*

1 Inu Aisraeli, imvani mawu a Yehova,

chifukwa Yehova ali ndi mlandu ndi inu
amene mumakhala m’dzikoli:
“M’dziko mwanu mulibe kukhulupirika, mulibe chikondi
mulibe kulabadira za Mulungu.
2 Muli kutemberera kokha, kunama ndi kupha.
Kuba ndi kuchita chigololo;
machimo achita kunyanya
ndipo akungokhalira kuphana.
3 Chifukwa chake dziko likulira
ndipo onse amene amakhalamo akuvutika;
zirombo zakuthengo ndi mbalame zamumlengalenga
ndiponso nsomba zam’nyanja zikufa.

4 “Koma wina asapeze mnzake chifukwa,
wina aliyense asayimbe mlandu mnzake,
pakuti anthu ako ali ngati anthu
amene amayimba mlandu wansembe.
5 Mumapunthwa usana ndi usiku
ndipo aneneri amapunthwa nanu pamodzi.
Choncho ndidzawononga amayi anu.
6 Anthu anga akuwonongeka chifukwa chosadziwa.

“Pakuti mwakana kudziwa,
Inenso ndidzakukanani monga ansembe anga;
chifukwa mwayiwala lamulo la Mulungu wanu,
Inenso ndidzayiwala ana anu.
7 Ansembe ankati akachuluka
iwo ankandichimwiranso kwambiri;
iwo anasinthanitsa ulemerero wawo ndi chinthu china chonyansa.
8 Amalemererapo pa machimo a anthu anga
ndipo amafunitsitsa kuti anthuwo azipitiriza kuchimwa.
9 Ndipo zidzakhala motere: zochitikira anthu ena, zidzachitikiranso ansembe.
Ndidzawalanga onsewo chifukwa cha njira zawo,
ndidzawabwezera chifukwa cha machitidwe awo.

10 “Iwo azidzadya koma sadzakhuta;
azidzachita zachiwerewere koma sadzachulukana,
chifukwa anasiya Yehova
kuti adzipereke 11 ku zachiwerewere,
ku vinyo wakale ndi watsopano,
zimene zimachotsa nzeru zomvetsa zinthu
12 za anthu anga.
Anthu anga amapempha nzeru ku fano lamtengo
ndipo ndodo yawo yamtengo imawayankha.
Mzimu wachiwerewere umawasocheretsa;
iwo sakukhulupirika kwa Mulungu wawo.
13 Amapereka nsembe pamwamba pa mapiri
ndi kufukiza lubani pa zitunda,
pa tsinde pa mtengo wa thundu, mnjale ndi mkundi,
pamene pali mthunzi wabwino.
N’chifukwa chake ana anu aakazi akuchita zachiwerewere

ndipo akazi a ana anu akuchita zigololo.

14 “Ine sindidzalanga ana anu aakazi
pamene iwo adzachita zachiwerewere,
kapena akazi a ana anu
pamene adzachita zigololo.
Paja inu nomwe amunanu mumayenda ndi akazi achiwerewere,
ndipo mumapereka nsembe pamodzi ndi akazi achiwerewere a ku malo opembedzerako.
Anthu amene alibe nzeru adzawonongeka ndithu!

15 “Ngakhale umachita chigololo, iwe Israeli,
Yuda asapezeke ndi mlandu wotere.

“Usapite ku Giligala.
Usapite ku Beti-Aveni.
Ndipo usalumbire kuti, ‘Pali Yehova wamoyo!’
16 Aisraeli ndi nkhutukumve,
ngosamva ngati ana ang’ombe.
Kodi Yehova angathe kuwaweta bwanji
ngati ana ankhosa pa msipu wabwino?
17 Efereimu waphathana ndi mafano;
mulekeni!
18 Ngakhale pamene zakumwa zawo zatha,
amapitiriza kuchita zachiwerewere;
atsogoleri awo amakonda kwambiri njira zawo zochititsa manyazi.
19 Adzachotsedwa ndi kamvuluvulu
ndipo adzachita manyazi chifukwa cha nsembe zawo.

# 5

*Chiweruzo cha Israeli*

1 “Ansembe inu, imvani izi!
Inu Aisraeli, tcherani khutu!
Inu nyumba yaufumu, mvetserani!
Chiweruzo ichi ndi chotsutsa inu:
Inu munali ngati msampha ku Mizipa,
munali ngati ukonde woyalidwa pa phiri la Tabori.
2 Owukira azama m’moyo wakupha,
Ine ndidzawalanga onsewo.
3 Ndimadziwa zonse za Efereimu;
Aisraeli ndi osabisika kwa Ine.
Efereimu wayamba tsopano kuchita zachiwerewere;
Israeli wadziyipitsa.

4 “Ntchito zawo siziwalola
kubwerera kwa Mulungu wawo.
M’mitima mwawo muli mzimu wachiwerewere;
Iwo sadziwa Yehova.
5 Kudzikuza kwa Israeli kwakhala umboni womutsutsa;
Aisraeli, ngakhale Aefereimu, anagwa m’machimo awo;
Yudanso anagwa nawo pamodzi.
6 Pamene adzapita ndi nkhosa zawo ndi ng’ombe zawo
kukapereka nsembe kwa Yehova,

iwo sadzamupeza;
Iye wawachokera.
7 Iwo ndi osakhulupirika kwa Yehova;
amabereka ana am'chigololo
ndipo chikondwerero chawo cha mwezi watsopano
chidzawawononga pamodzi ndi minda yawo.

8 "Womba lipenga mu Gibeya,
liza mbetete mu Rama.
Fuwulani mfuwu wankhondo mu Beti-Aveni;
iwe Benjamini tsogolera.
9 Efereimu adzasanduka bwinja
pa tsiku la chilango.
Ine ndikulengeza zomwe zidzachitikadi
pakati pa mafuko a Israeli.
10 Atsogoleri a Yuda ali ngati anthu
amene amasuntha miyala ya m'malire.
Ndidzawakhutulira ukali wanga
ngati madzi a chigumula.
11 Efereimu waponderezedwa,
akulangidwa chifukwa chotsatira
mafano.
12 Ine ndili ngati njenjete kwa Efereimu,
ngati chinthu chowola kwa anthu a ku Yuda.

13 "Efereimu ataona nthenda yake,
ndi Yuda ataona zilonda zake,
pamenepo Efereimu anatembenukira kwa Asiriya,
ndipo anawatumizira mfumu yayikulu kudzawathandiza.
Koma mfumuyo singathe kukuchizani,
singathe kuchiritsa mabala anu.
14 Pakuti Ine ndidzakhala ngati mkango kwa Efereimu.
Ngati mkango wamphamvu kwa Yuda.
Ndidzawakhadzula n'kuchokapo;
ndidzawatenga ndipo palibe amene adzawalanditse.
15 Ndipo ndidzabwerera ku malo anga
mpaka anthu anga atavomereza kulakwa kwawo.
Ndipo iwo adzafunafuna nkhope yanga;
m'masautso awo adzandifunitsitsa Ine."

# 6

*Kusalapa kwa Israeli*

1 "Bwerani, tiyeni tibwerere kwa Yehova.
Iye watikhadzula,
koma adzatichiritsa.
Iye wativulaza,
koma adzamanga mabala athu.
2 Pakapita masiku awiri adzatitsitsimutsa;
pa tsiku lachitatu Iye adzatiukitsa
kuti tikhale ndi moyo pamaso pake.
3 Tiyeni timudziwe Yehova,
tiyeni tilimbike kumudziwa Iye.

Adzabwera kwa ife mosakayikira konse
ngati kutuluka kwa dzuwa;
adzabwera kwa ife ngati mvula ya m'chilimwe,
ngati mvula ya nthawi yamphukira imene imakhathamiritsa nthaka."

4 Iwe Efereimu, kodi ndichite nawe chiyani?
Kodi ndichite nawe chiyani, iwe Yuda?
Chikondi chanu chili ngati nkhungu yammawa,
ngati mame a mmamawa amene amakamuka msanga.
5 Choncho ndakuwazani ngati nkhuni kudzera mwa aneneri anga,
ndakuphani ndi mawu a pakamwa panga;
chigamulo changa chinang'anima ngati mphenzi pa inu.
6 Pakuti Ine ndimafuna chifundo osati nsembe,
ndi kudziwa Mulungu kulekana ndi nsembe zopsereza.
7 Monga Adamu, anthuwa aphwanya pangano langa,
iwo sanakhulupirike kwa Ine.
8 Giliyadi ndi mzinda wa anthu ochita zoyipa,
okhala ndi zizindikiro za kuphana.
9 Monga momwe mbala zimadikirira anthu,
magulu a ansembe amachitanso motero;
iwo amapha anthu pa njira yopita ku Sekemu,
kupalamula milandu yochititsa manyazi.
10 Ndaona chinthu choopsa kwambiri
m'nyumba ya Israeli.
Kumeneko Efereimu akuchita zachiwerewere,
ndipo Israeli wadzidetsa.

11 "Kunenanso za iwe Yuda,
udzakolola chilango.

"Pamene ndiwabwezere anthu anga zinthu zabwino."

# 7

1 Pamene ndichiritsa Israeli,
machimo a Efereimu amaonekera poyera
ndiponso milandu ya Samariya sibisika.
Iwo amachita zachinyengo,
mbala zimathyola nyumba,
achifwamba amalanda anthu katundu m'misewu.
2 Koma sazindikira kuti Ine
ndimakumbukira zoyipa zawo zonse.
Azunguliridwa ndi zolakwa zawo;
ndipo sizichoka m'maso mwanga.

3 "Anthuwa amasangalatsa mfumu ndi zoyipa zawozo,
akalonga amasekerera mabodza awo.
4 Onsewa ndi anthu azigololo,
otentha ngati moto wa mu uvuni,
umene wophika buledi sasonkhezera
kuyambira pamene akukanda buledi mpaka atafufuma.
5 Pa tsiku la chikondwerero cha mfumu yathu
akalonga amaledzera ndi vinyo,

ndipo amalowa m'gulu la anthu achipongwe.
6 Mitima yawo ili ngati uvuni;
amayandikira Mulungu mwachiwembu.
Ukali wawo umanyeka usiku wonse,
mmawa umayaka ngati malawi a moto.
7 Onsewa ndi otentha ngati uvuni,
amapha olamulira awo.
Mafumu awo onse amagwa,
ndipo palibe ndi mmodzi yemwe amandiyitana Ine.

8 "Efereimu wasakanikirana ndi mitundu ya anthu ena;
Efereimu ndi buledi amene wapsa mbali imodzi.
9 Alendo atha mphamvu zake,
koma iye sakuzindikira.
Tsitsi lake layamba imvi
koma iye sakudziwa.
10 Kunyada kwake Israeli kukumutsutsa,
koma pa zonsezi
iye sakubwerera kwa Yehova Mulungu wake
kapena kumufunafuna.

11 "Efereimu ali ngati nkhunda
yopusa yopanda nzeru.
Amayitana Igupto
namapita ku Asiriya.
12 Akamadzapita, ndidzawakola ndi ukonde wanga;
ndidzawagwetsa pansi ngati mbalame zamumlengalenga.
Ndikadzamva kuti asonkhana pamodzi
ndidzawakola.
13 Tsoka kwa iwo,
chifukwa andisiya Ine!
Chiwonongeko kwa iwo,
chifukwa andiwukira!
Ndimafunitsitsa kuwapulumutsa
koma amayankhula za Ine monama.
14 Iwo salirira kwa Ine kuchokera pansi pa mtima,
koma amalira mofuwula ali pa bedi pawo.
Amadzichekacheka chifukwa chofuna tirigu ndi vinyo watsopano,
koma amandifulatira.
15 Ine ndinawaphunzitsa ndikuwalimbitsa,
koma amandikonzera chiwembu.
16 Iwo satembenukira kwa Wammwambamwamba;
ali ngati uta woonongeka.
Atsogoleri awo adzaphedwa ndi lupanga
chifukwa cha mawu awo achipongwe.
Motero iwo adzasekedwa
m'dziko la Igupto.

# 8

### *Israeli Akolola Kamvuluvulu*

1 "Ika lipenga pakamwa pako.
Ngati chiwombankhanga, kutsutsana ndi nyumba ya Yehova

chifukwa anthu aphwanya pangano langa
ndiponso agalukira lamulo langa.
2 Israeli akulirira kwa Ine kuti,
'Inu Mulungu wathu, ife timakudziwani!'
3 Koma Israeli wakana zabwino;
mdani adzamuthamangitsa.
4 Amalonga mafumu mosatsata kufuna kwanga.
Amasankha akalonga popanda chilolezo changa.
Amadzipangira mafano
asiliva ndi agolide
koma adzawonongeka nawo.
5 Iwe Samariya, taya fano lako la mwana wang'ombe!
Mkwiyo wanga wayakira anthuwo.
Padzapita nthawi yayitali chotani asanasinthike kukhala oyera mtima?
6 Mafanowa ndi ochokera ku Israeli!
Mwana wa ng'ombe uyu anapangidwa ndi munthu waluso;
si Mulungu amene anamupanga.
Adzaphwanyidwa n'kukhala zidutswa,
mwana wang'ombe wa ku Samariya.

7 "Aisraeli amadzala mphepo
ndipo amakolola kamvuluvulu.
Tirigu alibe ngala;
sadzabala chakudya.
Akanabala chakudya
alendo akanadya chakudyacho.
8 Israeli wamezedwa,
tsopano ali pakati pa anthu a mitundu ina
ngati chinthu cha chabechabe.
9 Pakuti iwo anapita ku Asiriya
ngati mbidzi yongodziyendera pa yokha.
Efereimu wadzigulitsa kwa zibwenzi zake.
10 Ngakhale wadzigulitsa pakati pa mitundu ya anthu,
Ine ndidzawasonkhanitsa pamodzi.
Iwo adzayamba kuzunzika pansi pa
ulamuliro wankhanza wa mfumu yamphamvu.

11 "Ngakhale Efereimu anamanga maguwa ambiri a nsembe zoperekedwa
chifukwa cha tchimo,
maguwa amenewa akhala malo ochimwirapo.
12 Ndinawalembera zinthu zambiri za malamulo anga,
koma iwo anaziyesa ngati zinthu zachilendo.
13 Amapereka nsembe za nyama kwa Ine
ndipo iwo amadya nyamayo,
koma Yehova sakondwera nazo.
Tsopano Iye adzakumbukira zoyipa zawo
ndi kuwalanga chifukwa cha machimo awo:
iwowo adzabwerera ku Igupto.
14 Israeli wayiwala Mlengi wake
ndipo wamanga nyumba zaufumu;
Yuda wachulukitsa mizinda ya malinga.
Koma Ine ndidzaponya moto pa mizinda yawoyo,

moto umene udzatenthe malinga awo.”

## 9

*Chilango cha Israeli*

1 Iwe Israeli, usakondwere;
monga imachitira mitundu ina.
Pakuti wakhala wosakhulupirika kwa Mulungu wako;
umakonda malipiro a chiwerewere
pa malo aliwonse opunthira tirigu.
2 Malo opunthira tirigu ndi malo opsinyira mphesa sadzadyetsa anthu;
adzasowa vinyo watsopano.
3 Sadzakhalanso m’dziko la Yehova.
Efereimu adzabwerera ku Igupto
ndipo mudzadya chakudya chodetsedwa ku Asiriya.
4 Iwo sadzaperekanso chopereka cha chakumwa kwa Yehova,
kapena nsembe zawo kuti akondweretse Yehovayo.
Nsembe zotere zidzakhala kwa iwo ngati chakudya cha anamfedwa;
onse akudya chakudya chimenechi adzakhala odetsedwa.
Chakudya ichi chidzakhala chodya okha,
sichidzalowa m’nyumba ya Yehova.

5 Kodi mudzachita chiyani pa tsiku la maphwando anu oyikika;
pa masiku a zikondwerero za Yehova?
6 Ngakhale iwo atathawa chiwonongeko,
Igupto adzawasonkhanitsa,
ndipo Mefisi adzawayika m’manda.
Khwisa adzamera pa ziwiya zawo zasiliva,
ndipo minga idzamera m’matenti awo.
7 Masiku achilango akubwera,
masiku obwezera ali pafupi.
Israeli adziwe zimenezi.
Chifukwa machimo anu ndi ochuluka kwambiri
ndipo udani wanu pa Mulungu ndi waukulu kwambiri.
Mneneri amamuyesa chitsiru,
munthu wanzeru za kwa Mulungu ngati wamisala.
8 Mneneri pamodzi ndi Mulungu wanga
ndiwo alonda a Efereimu,
koma mneneri amutchera misampha m’njira zake zonse,
ndipo udani ukumudikira m’nyumba ya Mulungu wake.
9 Iwo azama mu zachinyengo
monga masiku a Gibeya.
Mulungu adzakumbukira zolakwa zawo
ndipo adzawalanga chifukwa cha machimo awo.

10 “Pamene ndinamupeza Israeli
zinali ngati kupeza mphesa m’chipululu.
Nditaona makolo anu,
zinali ngati ndikuona nkhuyu zoyambirira kupsa.
Koma atafika ku Baala Peori,
anadzipereka ku fano lija lochititsa manyazi
ndipo anakhala onyansa ngati chinthu chimene anachikondacho.
11 Ulemerero wa Efereimu udzawuluka ngati mbalame.

Sipadzakhalanso kubereka ana, kuyembekezera kapena kutenga pathupi.
12 Ngakhale atalera ana
ndidzachititsa kuti mwana aliyense amwalire.
Tsoka kwa anthuwo
pamene Ine ndidzawafulatira!
13 Ndaona Efereimu ngati Turo,
atadzalidwa pa nthaka ya chonde.
Koma Efereimu adzatsogolera
ana ake kuti akaphedwe."

14 Inu Yehova, muwapatse.
Kodi mudzawapatsa chiyani?
Apatseni mimba yomangopita padera
ndi mawere owuma.

15 "Chifukwa cha zoyipa zawo zonse ku Giligala,
Ine ndinawada kumeneko.
Chifukwa cha machitidwe awo auchimo,
ndidzawapirikitsa m'nyumba yanga.
Sindidzawakondanso;
atsogoleri awo onse ndi owukira.
16 Efereimu wathedwa,
mizu yake yauma
sakubalanso zipatso.
Ngakhale atabereka ana,
Ine ndidzapha ana awo okondedwawo."

17 Mulungu wanga adzawakana
chifukwa sanamumvere Iye;
adzakhala oyendayenda pakati pa anthu a mitundu ina.

# 10

1 Israeli anali mpesa wotambalala;
anabereka zipatso zambiri.
Pamene zipatso zawo zinanka zichuluka,
anawonjezera kumanga maguwa ansembe.
Pamene dziko lake linkatukuka,
anakongoletsa miyala yake yopatulika.
2 Mtima wawo ndi wonyenga
ndipo tsopano ayenera kulangidwa chifukwa cha kulakwa kwawo.
Yehova adzagumula maguwa awo ansembe
ndi kuwononga miyala yawo yopatulika.

3 Pamenepo anthuwo adzanena kuti, "Ife tilibe mfumu
chifukwa sitinaope Yehova.
Koma ngakhale tikanakhala ndi mfumu,
kodi mfumuyo ikanatichitira chiyani?"
4 Mafumu amalonjeza zambiri,
amalumbira zabodza
pochita mapangano.
Kotero maweruzo amaphuka

ngati zitsamba zakupha m'munda umene walimidwa.
5 Anthu amene amakhala mu Samariya akuchita mantha
chifukwa cha fano la mwana wang'ombe ku Beti-Aveni.
Anthu ake adzalirira fanolo,
chimodzimodzinso ansembe ake adamawo,
amene anakondwera ndi kukongola kwake,
chifukwa lachotsedwa pakati pawo ndi kupita ku ukapolo.
6 Fanolo lidzatengedwa kupita ku Asiriya
ngati mphatso kwa mfumu yayikulu.
Efereimu adzachititsidwa manyazi
chifukwa cha mafano ake amitengo.
7 Samariya ndi mfumu yake adzatengedwa kupita kutali
ngati kanthambi koyenda pa madzi.
8 Malo opembedzerako mafano a ku Aveni adzawonongedwa.
Ili ndiye tchimo la Israeli.
Minga ndi mitungwi zidzamera
ndi kuphimba maguwa awo ansembe.
Kenaka anthu adzawuza mapiri kuti, "Tiphimbeni!"
ndipo adzawuza zitunda kuti, "Tigwereni!"

9 "Iwe Israeli, wachimwa kuyambira m'masiku a Gibeya,
ndipo wakhala uli pomwepo.
Kodi nkhondo sinagonjetse anthu
ochita zoyipa ku Gibeya?
10 Pamene ndifunire, ndidzalanga anthuwo;
mitundu ya anthu idzasonkhanitsidwa kudzalimbana nawo,
kuwayika m'ndende chifukwa cha uchimo wawo waukulu.
11 Efereimu ndi mwana wang'ombe wamkazi wophunzitsidwa
amene amakonda kupuntha tirigu,
choncho Ine ndidzayika goli
m'khosi lake lokongolalo.
Ndidzasenzetsa Efereimu goli,
Yuda ayenera kulima,
ndipo Yakobo ayenera kutipula.
12 Mufese nokha chilungamo
ndipo mudzakolola chipatso cha chikondi changa chosasinthika.
Ndipo tipulani munda wanu wosalimidwawo;
pakuti ino ndi nthawi yofunafuna Yehova,
mpaka Iye atabwera
kudzakugwetserani mivumbi ya chilungamo.
13 Koma inu munadzala zolakwa,
mwakolola zoyipa;
mwadya chipatso cha chinyengo.
Chifukwa mumadalira mphamvu zanu
ndiponso ankhondo anu ochulukawo,
14 phokoso lankhondo lidzamveka pakati pa anthu anga
kotero kuti malinga anu onse adzawonongeka,
monga momwe Salimani anawonongera Beti-Aribeli pa nthawi ya nkhondo;
pamene anapha amayi pamodzi ndi ana awo omwe.
15 Momwemonso zidzakuchitikira, iwe Beteli
chifukwa kuyipa kwako ndi kwakukulu.

Tsiku limeneli likadzafika,
mfumu ya Israeli idzawonongedwa kwathunthu.

# 11

*Chikondi cha Mulungu pa Israeli*

1 "Israeli ali mwana, ndinamukonda,
ndipo ndinayitana mwana wanga kuti atuluke mu Igupto.
2 Koma ndimati ndikamapitiriza kuyitana
iwo amandithawa kupita kutali.
Ankapereka nsembe kwa Abaala
ndipo ankafukiza lubani kwa mafano.
3 Ndi Ine amene ndinaphunzitsa Efereimu kuyenda,
ndipo ndinawagwira pa mkono;
koma iwo sanazindikire
kuti ndine amene ndinawachiritsa.
4 Ndinawatsogolera ndi zingwe zachifundo cha anthu
ndi zomangira za chikondi;
ndinachotsa goli m'khosi mwawo
ndipo ndinawerama n'kuwadyetsa.

5 "Sadzabwerera ku Igupto,
koma Asiriya ndiye adzakhala mfumu yawo
pakuti akana kutembenuka.
6 Malupanga adzang'anima m'mizinda yawo,
ndipo adzawononga mipiringidzo ya zipata zawo
nadzathetseratu malingaliro awo.
7 Anthu anga atsimikiza zondifulatira Ine.
Ngakhale atayitana Wammwambamwamba,
sizidzatheka kuti Iye awakwezenso.

8 "Kodi ndingakusiye bwanji iwe Efereimu?
Kodi ndingakupereke bwanji iwe Israeli?
Kodi ndingakuchitire bwanji zimene ndinachitira Adima?
Kodi ndingathe bwanji kukuchitira zimene ndinachitira Zeboimu?
Mtima wanga wakana kutero;
chifundo changa chonse chikusefukira.
9 Sindidzalola kuti ndikulange ndi mkwiyo wanga woopsa,
kapena kutembenuka ndi kuwononga Efereimu.
Pakuti Ine ndine Mulungu osati munthu,
Woyerayo pakati panu.
Sindidzabwera mwaukali.
10 Iwo adzatsatira Yehova;
Iye adzabangula ngati mkango.
Akadzabangula,
ana ake adzabwera akunjenjemera kuchokera kumadzulo.
11 Adzabwera akunjenjemera
ngati mbalame kuchokera ku Igupto,
ngati nkhunda kuchokera ku Asiriya.
Ine ndidzawakhazikanso m'nyumba zawo,"
akutero Yehova.

*Tchimo la Israeli*

12 Efereimu wandizungulira ndi mabodza,

nyumba ya Israeli yandizungulira ndi chinyengo.
Ndipo Yuda wawukira Mulungu,
wawukira ngakhale Woyerayo amene ndi wokhulupirika.

## 12

1 Efereimu amadya mpweya;
tsiku lonse amasaka mphepo ya kummawa
ndipo amachulukitsa mabodza ndi chiwawa.
Amachita mgwirizano ndi Asiriya
ndipo amatumiza mphatso za mafuta a olivi ku Igupto.
2 Yehova akuyimba mlandu Yuda;
Iye adzalanga Yakobo molingana ndi makhalidwe ake,
adzamulanga molingana ndi ntchito zake.
3 Akali m'mimba mwa amayi ake, Yakobo anagwira chidendene cha m'bale wake;
iye atakula analimbana ndi Mulungu.
4 Yakobo analimbana ndi mngelo ndipo anapambana;
analira napempha kuti amukomere mtima.
Mulungu anakumana naye ku Beteli
ndipo anayankhula naye kumeneko,
5 Yehova Mulungu Wamphamvuzonse,
Yehova ndiye dzina lake lotchuka!
6 Koma inu muyenera kubwerera kwa Mulungu wanu;
pitirizani chikondi ndi chiweruzo cholungama,
ndipo muzidikira Mulungu wanu nthawi zonse.

7 Munthu wamalonda amagwiritsa ntchito masikelo achinyengo;
iyeyo amakonda kubera anthu.
8 Efereimu amadzitama ponena kuti,
"Ndine wolemera kwambiri; ndili ndi chuma chambiri.
Palibe amene angandiloze chala
chifukwa cha kulemera kwanga."

9 "Ine ndine Yehova Mulungu wako
amene ndinakutulutsa mu Igupto.
Ndidzakukhazikaninso m'matenti,
monga munkachitira masiku aja pa nthawi ya zikondwerero zanu.
10 Ndinayankhula ndi aneneri,
ndinawaonetsa masomphenya ambiri,
ndipo ndinawawuza mafanizo kudzera mwa iwo."

11 Kodi Giliyadi ndi woyipa?
Anthu ake ndi achabechabe!
Kodi amapereka nsembe za ng'ombe zazimuna ku Giligala?
Maguwa awo ansembe adzakhala ngati milu ya miyala
m'munda molimidwa.
12 Yakobo anathawira ku dziko la Aramu,
Israeli anagwira ntchito kuti apeze mkazi,
ndipo anaweta nkhosa kuti akwatire mkaziyo.
13 Yehova anagwiritsa ntchito mneneri kuti atulutse Israeli mu Igupto;
kudzera mwa mneneriyo Iye anawasamalira.
14 Koma Efereimu wamukwiyitsa kwambiri.

N'chifukwa chake Yehova adzawalanga ndi imfa.
Adzawalanga chifukwa anamuchititsa manyazi kwambiri.

# 13

*Mkwiyo wa Yehova pa Israeli*

1 Kale Efereimu ankati akayankhula, anthu ankanjenjemera;
anali wolemekezeka mu Israeli.
Koma analakwa popembedza Baala, motero anafa.
2 Tsopano akunka nachimwirachimwirabe;
akudzipangira mafano pogwiritsa ntchito siliva wawo,
zifanizo zopangidwa mwaluso,
zonsezo zopangidwa ndi amisiri.
Amanena za anthu awa kuti,
"Amatenga munthu ndi kumupereka nsembe
ndipo amapsompsona fano la mwana wang'ombe."
3 Choncho adzakhala ngati nkhungu yammawa,
ngati mame amene amakamuka msanga,
ngati mungu wowuluka kuchokera pa malo opunthira tirigu,
ngati utsi umene ukutulukira pa zenera.

4 Koma Ine ndine Yehova Mulungu wanu,
amene ndinakutulutsani mu Igupto.
Simuyenera kudziwa Mulungu wina, koma Ine ndekha,
palibe Mpulumutsi wina kupatula Ine.
5 Ndinakusamalira m'chipululu,
m'dziko lotentha kwambiri.
6 Pamene ndinawadyetsa, iwo anakhuta;
iwo atakhuta anayamba kunyada;
ndipo anandiyiwala Ine.
7 Motero ndidzawalumphira ngati mkango,
ndidzawabisalira mu msewu ngati kambuku.
8 Ngati chimbalangondo cholandidwa ana ake,
ndidzawambwandira ndi kuwathyolathyola.
Ndidzawapwepweta ngati mkango;
chirombo chakuthengo chidzawakhadzula.

9 "Iwe Israeli, wawonongedwa,
chifukwa ukutsutsana ndi Ine, ukutsutsana ndi mthandizi wako.
10 Kodi mfumu yako ili kuti, kuti ikupulumutse?
Olamulira ako a m'mizinda yonse ali kuti,
amene iwe unanena za iwo kuti,
'Patseni mfumu ndi akalonga?'
11 Choncho Ine ndinakupatsani mfumu mwachipseramtima,
ndipo ndinayichotsa mwaukali.
12 Kulakwa kwa Efereimu kwasungidwa,
machimo ake alembedwa m'buku.
13 Zowawa zonga za mayi pa nthawi yobala mwana zamugwera,
koma iye ndi mwana wopanda nzeru,
pamene nthawi yake yobadwa yafika
iyeyo safuna kutuluka m'mimba mwa amayi ake.

14 “Ndidzawapulumutsa ku mphamvu ya manda;
ndidzawawombola ku imfa.
Kodi iwe imfa, miliri yako ili kuti?
Kodi iwe manda, kuwononga kwako kuli kuti?

“Sindidzachitanso chifundo,
15 ngakhale Efereimu akondwe pakati pa abale ake,
mphepo ya kummawa yochokera kwa Yehova idzabwera,
ikuwomba kuchokera ku chipululu.
Kasupe wake adzaphwa
ndipo chitsime chake chidzawuma.
Chuma chake chonse chamtengowapatali
chidzafunkhidwa ndipo chidzatengedwa.
16 Anthu a ku Samariya adzalangidwa chifukwa cha zolakwa zawo,
chifukwa anawukira Mulungu wawo.
Adzaphedwa ndi lupanga;
ana awo adzaphedwa mowamenyetsa pansi,
akazi awo oyembekezera adzatumbulidwa pa mimba.”

# 14

*Kulapa Kubweretsa Madalitso*

1 Iwe Israeli bwerera kwa Yehova Mulungu wako.
Machimo anu ndi amene akugwetsani!
2 Bweretsani zopempha zanu
ndipo bwererani kwa Yehova.
Munene kwa Iye kuti,
“Tikhululukireni machimo athu onse
ndi kutilandira mokoma mtima,
kuti tithe kukuyamikani ndi mawu a pakamwa pathu.
3 Asiriya sangatipulumutse;
ife sitidzakwera pa akavalo ankhondo,
sitidzanenanso kuti, ‘Milungu yathu’
kwa zimene manja athu omwe anazipanga,
pakuti ndinu amene mumachitira chifundo ana amasiye.”

4 Ine ndidzachiza kusakhulupirika kwawo
ndipo ndidzawakonda mwaufulu
pakuti ndaleka kuwakwiyira.
5 Ndidzakhala ngati mame kwa Israeli
Ndipo iye adzachita maluwa ngati kakombo.
Adzazika mizu yake pansi
ngati mkungudza wa ku Lebanoni;
6 mphukira zake zidzakula.
Kukongola kwake kudzakhala ngati mtengo wa olivi,
kununkhira kwake ngati mkungudza wa ku Lebanoni.
7 Anthu adzakhalanso mu mthunzi wake.
Iye adzakula bwino ngati tirigu.
Adzachita maluwa ngati mphesa
ndipo kutchuka kwake kudzakhala ngati vinyo wochokera ku Lebanoni.
8 Efereimu adzati, “Ndidzachita nawonso chiyani mafano?
Ine ndidzamuyankha ndi kumusamalira.

Ine ndili ngati mtengo wa payini wobiriwira;
zipatso zako zimachokera kwa Ine.”

9 Ndani ali ndi nzeru? Adzazindikire zinthu izi.
Ndani amene amamvetsa zinthu? Adzamvetse izi.
Njira za Yehova ndi zolungama;
anthu olungama amayenda m’menemo,
koma anthu owukira amapunthwamo.

# Yoweli

1 Yehova anayankhula ndi Yoweli mwana wa Petueli.

*Kubwera kwa Dzombe*

2 Inu akuluakulu, imvani izi;
mvetserani, nonse amene mumakhala m'dziko.
Kodi zinthu zokhala ngati izi zinayamba zaonekapo m'nthawi yanu,
kapena m'nthawi ya makolo anu?
3 Muwafotokozere ana anu,
ndipo ana anuwo afotokozere ana awo,
ndipo ana awo adzafotokozere m'bado winawo.
4 Chimene dzombe losamera mapiko lasiya
dzombe lowuluka ladya;
chimene dzombe lowuluka lasiya
dzombe laling'ono ladya;
chimene dzombe laling'ono lasiya
chilimamine wadya.

5 Dzukani, inu zidakwa ndipo mulire!
Lirani mofuwula, inu nonse amene mumamwa vinyo;
lirani mofuwula chifukwa cha vinyo watsopano,
pakuti wachotsedwa pakamwa panu.
6 Mtundu wa anthu wathira nkhondo dziko langa,
wamphamvu ndi wosawerengeka;
uli ndi mano a mkango,
zibwano za mkango waukazi.
7 Wawononga mphesa zanga
ndipo wathyola mitengo yanga ya mkuyu.
Wakungunula makungwa ake
ndi kuwataya,
kusiya nthambi zake zili mbee.

8 Lirani ngati namwali wovala chiguduli,
chifukwa cha mwamuna wa utsikana wake.
9 Chopereka cha chakudya ndi cha chakumwa
sizikuperekedwa ku nyumba ya Yehova.
Ansembe akulira,
amene amatumikira pamaso pa Yehova.
10 Minda yaguga,
nthaka yauma;
tirigu wawonongeka,
vinyo watsopano watha,
mitengo ya mafuta yauma.
11 Khalani ndi nkhawa, inu alimi,
lirani mofuwula inu alimi a mphesa;
imvani chisoni chifukwa cha tirigu ndi barele,
pakuti zokolola za m'munda zawonongeka.
12 Mpesa wauma
ndipo mtengo wamkuyu wafota;
makangadza, kanjedza ndi mitengo ya apulosi,

mitengo yonse ya m'munda yauma.
Ndithudi chimwemwe cha anthu
chatheratu.

*Mulungu Ayitana Anthu kuti Atembenuke*

13 Inu ansembe, valani ziguduli ndipo lirani;
lirani mofuwula, inu amene mumatumikira pa guwa lansembe.
Bwerani, fundani ziguduli usiku wonse,
inu amene mumatumikira pamaso pa Mulungu wanga;
pakuti chopereka cha chakudya ndi cha chakumwa
sizikupezekanso m'nyumba ya Mulungu wanu.
14 Lengezani tsiku lopatulika losala zakudya,
itanani msonkhano wopatulika.
Sonkhanitsani akuluakulu
ndi anthu onse okhala m'dziko
ku nyumba ya Yehova Mulungu wanu
ndipo alirire Yehova.

15 Kalanga ine tsikulo!
Pakuti tsiku la Yehova layandikira;
lidzabwera ngati chiwonongeko chochokera kwa Wamphamvuzonse.

16 Kodi chakudya chathu sichachotsedwa
ife tikuona?
Kodi m'nyumba ya Mulungu wathu
simulibe chimwemwe ndi chisangalalo?
17 Mbewu zikunyala
poti pansi ndi powuma.
Nyumba zosungiramo zinthu zawonongeka;
nkhokwe zapasuka
popeza tirigu wauma.
18 Taonani mmene zikulirira ziweto;
ng'ombe zikungoyenda uku ndi uku
chifukwa zilibe msipu;
ngakhalenso nkhosa zikusauka.

19 Kwa Inu Yehova ndilirira,
pakuti moto wapsereza msipu wakuthengo,
malawi amoto apsereza mitengo yonse ya m'tchire.
20 Ngakhale nyama zakuthengo zikulirira Inu;
timitsinje tonse taphwa
ndipo moto wapsereza msipu wa kuthengo.

# 2

*Chilango cha Mulungu*

1 Lizani lipenga mu Ziyoni.
Chenjezani pa phiri langa loyera.
Onse okhala m'dziko anjenjemere,
pakuti tsiku la Yehova likubwera,
layandikira;
2 tsiku la mdima ndi chisoni,
tsiku la mitambo ndi la mdima wandiweyani.

Ngati m'bandakucha umene wakuta mapiri,
gulu lalikulu ndi la ankhondo amphamvu likubwera,
gulu limene n'kale lomwe silinaonekepo
ngakhale kutsogolo kuno silidzaonekanso.
3 Patsogolo pawo moto ukupsereza,
kumbuyo kwawo malawi amoto akutentha zinthu.
Patsogolo pawo dziko lili ngati munda wa Edeni,
kumbuyo kwawo kuli ngati chipululu,
kulibe kanthu kotsalapo.
4 Maonekedwe awo ali ngati akavalo;
akuthamanga ngati akavalo ankhondo.
5 Akulumpha pamwamba pa mapiri
ndi phokoso ngati la magaleta,
ngati moto wothetheka wonyeketsa ziputu,
ngati gulu lalikulu la ankhondo lokonzekera nkhondo.

6 Akangowaona, anthu a mitundu ina amazunzika mu mtima;
nkhope iliyonse imagwa.
7 Amathamanga ngati ankhondo;
amakwera makoma ngati asilikali.
Onse amayenda pa mizere,
osaphonya njira yawo.
8 Iwo sakankhanakankhana,
aliyense amayenda molunjika.
Amadutsa malo otchingidwa
popanda kumwazikana.
9 Amakhamukira mu mzinda,
amathamanga m'mbali mwa khoma.
Amakwera nyumba ndi kulowamo;
amalowera pa zenera ngati mbala.

10 Patsogolo pawo dziko limagwedezeka,
thambo limanjenjemera,
dzuwa ndi mwezi zimachita mdima,
ndipo nyenyezi zimaleka kuwala.
11 Yehova amabangula
patsogolo pawo,
gulu lake lankhondo ndi losawerengeka,
ndipo amphamvu ndi amene amamvera kulamula kwake.
Tsiku la Yehova ndi lalikulu;
ndi loopsa.
Ndani adzapirira pa tsikulo?

### *Ng'ambani Mtima Wanu*

12 "Ngakhale tsopano,
bwererani kwa Ine ndi mtima wanu wonse
posala zakudya ndi kukhetsa misozi," akutero Yehova.

13 Ng'ambani mtima wanu
osati zovala zanu.
Bwererani kwa Yehova Mulungu wanu,
pakuti Iye ndi wokoma mtima ndi wachifundo,
wosakwiya msanga ndi wachikondi chochuluka,

ndipo amaleka kubweretsa mavuto.
14 Akudziwa ndani? Mwina adzasintha maganizo n'kutimvera chisoni,
n'kutisiyira madalitso,
a chopereka cha chakudya ndi cha chakumwa
kwa Yehova Mulungu wanu.

15 Lizani lipenga mu Ziyoni,
lengezani tsiku losala zakudya,
itanitsani msonkhano wopatulika.
16 Sonkhanitsani anthu pamodzi,
muwawuze kuti adziyeretse;
sonkhanitsani akuluakulu,
sonkhanitsani ana,
sonkhanitsani ndi oyamwa omwe.
Mkwati atuluke m'chipinda chake,
mkwatibwi atuluke mokhala mwake.
17 Ansembe amene amatumikira pamaso pa Yehova,
alire pakati pa guwa lansembe ndi khonde la Nyumba ya Yehova.
Azinena kuti, “Inu Yehova, achitireni chifundo anthu anu.
Musalole kuti cholowa chanu chikhale chinthu chonyozeka,
kuti anthu a mitundu ina awalamulire.
Kodi n'chifukwa chiyani anthu a mitundu ina amanena kuti,
‘Ali kuti Mulungu wawo?’ ”

*Yankho la Yehova*

18 Pamenepo Yehova adzachitira nsanje dziko lake
ndi kuchitira chisoni anthu ake.
19 Yehova adzawayankha kuti,
“Ine ndikukutumizirani tirigu, vinyo watsopano ndi mafuta
ndipo mudzakhuta ndithu;
sindidzakuperekaninso kuti mukhale chitonzo
kwa anthu a mitundu ina.

20 “Ine ndidzachotsa ankhondo akumpoto kuti apite kutali ndi inu,
kuwapirikitsira ku dziko lowuma ndi lachipululu,
gulu lawo lakutsogolo ndidzalipirikitsira ku nyanja ya kummawa
ndi gulu lawo lakumbuyo, ku nyanja ya kumadzulo.
Ndipo mitembo yawo idzawola,
fungo lake lidzamveka.”

Zoonadi Yehova wachita zinthu zazikulu.
21 Iwe dziko usachite mantha;
sangalala ndipo kondwera.
Zoonadi Yehova wachita zinthu zazikulu.
22 Inu nyama zakuthengo, musachite mantha,
pakuti msipu wa ku chipululu ukuphukira.
Mitengo ikubala zipatso zake;
mitengo ya mkuyu ndi mpesa ikubereka kwambiri.
23 Inu anthu a ku Ziyoni sangalalani,
kondwerani mwa Yehova Mulungu wanu,
pakuti wakupatsani
mvula yoyambirira mwachilungamo chake.
Iye wakutumizirani mivumbi yochuluka,

mvula yoyambirira ndi mvula ya nthawi ya mphukira, monga poyamba paja.
24 Pa malo opunthira padzaza tirigu;
m'mitsuko mudzasefukira vinyo watsopano ndi mafuta.

25 “Ine ndidzakubwezerani zonse zimene zinawonongedwa ndi dzombe,
dzombe lalikulu ndi dzombe laling'ono,
dzombe lopanda mapiko ndi dzombe lowuluka;
gulu langa lalikulu la nkhondo limene ndinalitumiza pakati panu.
26 Mudzakhala ndi chakudya chambiri, mpaka mudzakhuta,
ndipo mudzatamanda dzina la Yehova Mulungu wanu,
amene wakuchitirani zodabwitsa;
ndipo anthu anga sadzachitanso manyazi.
27 Pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine ndili mu Israeli,
kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu,
ndi kuti palibenso wina;
ndipo anthu anga sadzachitanso manyazi.

*Tsiku la Yehova*

28 “Ndipo patapita nthawi,
ndidzakhuthulira Mzimu wanga pa anthu onse.
Ana anu aamuna ndi ana anu aakazi adzanenera,
nkhalamba zanu zidzalota maloto,
anyamata anu adzaona masomphenya.
29 Ngakhalenso pa antchito anga aamuna ndi aakazi
ndidzakhuthulira Mzimu wanga masiku amenewo.
30 Ndidzaonetsa zodabwitsa mlengalenga
ndi pa dziko lapansi,
ndizo magazi, moto ndi utsi watolotolo.
31 Dzuwa lidzadetsedwa
ndipo mwezi udzaoneka ngati magazi
lisanafike tsiku lalikulu ndi loopsa la Ambuye.
32 Ndipo aliyense amene adzayitana
pa dzina la Ambuye adzapulumuka;
pakuti chipulumutso chidzakhala pa Phiri la Ziyoni
ndi mu Yerusalemu,
monga Yehova wanenera,
pakati pa otsala
amene Yehova wawayitana.

# 3

*Kuweruzidwa kwa Mitundu ya Anthu*

1 “Masiku amenewo ndiponso nthawi imeneyo,
nditadzabwezeretsanso Yerusalemu ndi Yuda m'chimake,
2 ndidzasonkhanitsa anthu a mitundu yonse
ndipo ndidzawabweretsa ku Chigwa cha Yehosafati.
Kumeneko ndidzawaweruza
chifukwa cha cholowa changa, anthu anga Aisraeli,
pakuti anabalalitsa anthu anga pakati pa mitundu ya anthu
ndikugawa dziko langa.
3 Anagawana anthu anga pochita maere
ndipo anyamata anawasinthanitsa ndi akazi achiwerewere;

anagulitsa atsikana chifukwa cha vinyo
kuti iwo amwe.
4 “Kodi tsopano inu a ku Turo ndi Sidoni ndi madera onse a Filisitiya,
muli ndi chiyani chotsutsana nane? Kodi mukundibwezera pa zinthu
zimene ndakuchitirani? Ngati inu mukundibwezera, Ine ndidzabwezera
zochita zanu mofulumira ndi mwachangu pa mitu yanu. 5 Pakuti
munatenga siliva ndi golide wanga ndi kupita nacho chuma changa
chamtengowapatali ku nyumba zanu zopembedzera mafano. 6 Inu
munagulitsa anthu a ku Yuda ndi Yerusalemu kwa Agriki, kuti apite kutali
ndi malire a dziko lawo.
7 “Taonani, Ine ndidzawachotsa kumalo kumene munawagulitsako,
ndipo ndidzabwezera zimene mwachita pa mitu yanu. 8 Ndidzagulitsa
ana anu aamuna ndi ana anu aakazi kwa anthu a ku Yuda, ndipo iwo
adzawagulitsa kwa Aseba, mtundu wa anthu okhala kutali.” Yehova
wayankhula.

9 Lengezani izi pakati pa anthu a mitundu ina:
Konzekerani nkhondo!
Dzutsani ankhondo amphamvu!
Asilikali onse afike pafupi ndipo ayambe nkhondo.
10 Sulani makasu anu kuti akhale malupanga
ndipo zikwanje zanu zikhale mikondo.
Munthu wofowoka anene kuti,
“Ndine wamphamvu!”
11 Bwerani msanga, inu anthu a mitundu yonse kuchokera ku mbali zonse,
ndipo musonkhane kumeneko.

Tumizani ankhondo anu Yehova!

12 “Mitundu ya anthu idzuke;
ipite ku Chigwa cha Yehosafati,
pakuti kumeneko Ine ndidzakhala
ndikuweruza anthu a mitundu yonse yozungulira.
13 Tengani chikwakwa chodulira tirigu,
pakuti mbewu zakhwima.
Bwerani dzapondeni mphesa,
pakuti mopsinyira mphesa mwadzaza
ndipo mitsuko ikusefukira;
kuyipa kwa anthuwa n’kwakukulu kwambiri!”

14 Chigulu cha anthu, chigulu cha anthu,
m’chigwa cha chiweruzo!
Pakuti tsiku la Yehova layandikira
m’chigwa cha chiweruzo.
15 Dzuwa ndi mwezi zidzadetsedwa,
ndipo nyenyezi sizidzawalanso.
16 Yehova adzabangula kuchokera mu Ziyoni
ndipo mawu ake adzamveka ngati bingu kuchokera mu Yerusalemu;
dziko lapansi ndi thambo zidzagwedezeka.
Koma Yehova adzakhala pothawira pa anthu ake,
linga la anthu a ku Israeli.

### *Madalitso a Anthu a Mulungu*

17 “Pamenepo inu mudzadziwa kuti Ine Yehova Mulungu wanu,

ndimakhala mu Ziyoni, phiri langa lopatulika.
Yerusalemu adzakhala wopatulika;
alendo sadzamuthiranso nkhondo.

18 “Tsiku limenelo mapiri adzachucha vinyo watsopano,
ndipo zitunda zidzayenderera mkaka;
mitsinje yonse ya ku Yuda idzadzaza ndi madzi.
Kasupe adzatumphuka m’nyumba ya Yehova
ndipo adzathirira Chigwa cha Sitimu.
19 Koma Igupto adzasanduka bwinja,
Edomu adzasanduka chipululu,
chifukwa cha nkhondo imene anathira anthu a ku Yuda
m’dziko limene anakhetsa magazi a anthu osalakwa.
20 Koma Yuda adzakhala ndi anthu mpaka muyaya
ndi Yerusalemu ku mibadomibado.
21 Kukhetsa magazi kwawo kumene Ine sindinakhululuke
ndidzakhululuka.”

Yehova amakhala mu Ziyoni!

# Amosi

1 Mawu a Amosi, mmodzi mwa anthu oweta nkhosa ku Tekowa. Zimene
iye anaona m'masomphenya zokhudza Israeli patatsala zaka ziwiri kuti
chivomerezi chichitike, nthawi imene Uziya anali mfumu ya Yuda ndipo
Yeroboamu mwana wa Yowasi anali mfumu ya Israeli.
2 Amosi anati:
"Yehova akubangula mu Ziyoni
ndipo akumveka ngati bingu mu Yerusalemu;
msipu wa abusa ukulira,
ndipo pamwamba pa Karimeli pakuwuma."

*Chiweruzo pa Anthu Oyandikana ndi Israeli*

3 Yehova akuti,
"Chifukwa anthu a ku Damasiko akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Popeza anapuntha Giliyadi
ndi zopunthira za mano achitsulo,
4 Ine ndidzatumiza moto pa nyumba ya Hazaeli
umene udzanyeketsa nyumba zaufumu za Beni-Hadadi.
5 Ndidzathyola chipata cha Damasiko;
ndidzawononga mfumu yokhala ku Chigwa cha Aveni,
ndiponso iye amene akugwira ndodo yaufumu mu Beti-Edeni.
Anthu a ku Aramu adzapita ku ukapolo ku Kiri,"
akutero Yehova.
6 Yehova akuti,
"Chifukwa anthu a ku Gaza akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Popeza anatenga ukapolo mtundu wathunthu
ndi kuwugulitsa ku Edomu,
7 ndidzatumiza moto pa makoma a Gaza
umene udzanyeketsa nyumba zake zaufumu.
8 Ndidzawononga mfumu ya ku Asidodi
komanso amene akugwira ndodo yaufumu ku Asikeloni.
Ndidzalanga Ekroni,
mpaka wotsala mwa Afilisti atafa,"
akutero Ambuye Yehova.
9 Yehova akuti,
"Chifukwa anthu a ku Turo akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Popeza iwo anagulitsa mtundu wathunthu ku ukapolo ku Edomu,
osasunga pangano laubale lija,
10 Ine ndidzatumiza moto pa makoma a Turo
umene udzanyeketsa nyumba zake zaufumu."
11 Yehova akuti,
"Chifukwa anthu a ku Edomu akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Popeza anathamangitsa m'bale wake ndi lupanga,
popanda n'chifundo chomwe.
Popeza mkwiyo wake unakulabe

ndipo ukali wake sunatonthozeke,
12 Ine ndidzatumiza moto pa Temani
umene udzanyeketsa nyumba zaufumu za Bozira.”
13 Yehova akuti,
“Chifukwa anthu a ku Amoni akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Popeza anatumbula akazi oyembekezera a ku Giliyadi
n’cholinga choti akuze malire awo,
14 Ine ndidzayatsa moto pa makoma a ku Raba
umene udzanyeketsa nyumba zake zaufumu.
Padzakhala kulira kwakukulu pa tsiku la nkhondoyo,
kumenyana kudzakhala kwafumbi ngati mkuntho wa kamvuluvulu.
15 Mfumu yawo idzatengedwa kupita ku ukapolo,
iyo pamodzi ndi akuluakulu ake,”
akutero Yehova.

# 2

1 Yehova akuti,
“Chifukwa anthu a ku Mowabu akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Popeza anatentha mafupa a mfumu ya ku Edomu,
mpaka kuwasandutsa phulusa,
2 Ine ndidzatumiza moto pa Mowabu,
umene udzanyeketsa nyumba zaufumu za ku Keriyoti.
Mowabu adzafera pakati pa nkhondo yoopsa,
m’kati mwa mfuwu wa nkhondo ndi kuliza malipenga.
3 Ndidzawononga wolamulira wake
ndi kupha akuluakulu onse amene ali pamodzi ndi iye,”
akutero Yehova.
4 Yehova akuti,
“Chifukwa anthu a ku Yuda akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Popeza iwo akana lamulo la Yehova
ndipo sanasunge malangizo ake,
popeza asocheretsedwa ndi milungu yabodza,
milungu imene makolo awo ankayitsatira,
5 Ine ndidzatumiza moto pa Yuda,
umene udzanyeketsa nyumba zaufumu za ku Yerusalemu.”

### *Chilango cha Anthu a ku Israeli*

6 Yehova akuti,
“Chifukwa anthu a ku Israeli akunka nachimwirachimwira,
Ine sindileka kuwalanga.
Iwo amagulitsa anthu olungama ndi siliva,
ndi osauka ndi nsapato.
7 Amapondereza anthu osauka
ngati akuponda fumbi,
ndipo sawaweruza mwachilungamo anthu oponderezedwa.
Abambo ndi mwana wawo amagonana ndi mtsikana mmodzi yemweyo,
ndipo potero amanyozetsa dzina langa loyera.
8 Anthuwo amakagonana m’mbali mwa guwa lililonse la nsembe
pa zovala zimene anatenga ngati chikole.
M’nyumba ya mulungu wawo

amamweramo vinyo amene analipiritsa anthu pa milandu.

9 “Ine ndinawononga Aamori pamaso pawo,
ngakhale iwo anali anthu ataliatali ngati mikungudza
ndiponso amphamvu ngati mitengo ya thundu.
Ndinawononga zipatso zawo
ndiponso mizu yawo.

10 “Ine ndinakutulutsani ku Igupto,
ndipo ndinakutsogolerani m’chipululu kwa zaka makumi anayi,
kudzakupatsani dziko la Aamori.
11 Ine ndinawutsanso ena mwa ana ako kuti akhale aneneri,
ndi ena mwa anyamata ako kuti akhale anaziri.
Kodi si choncho, inu Aisraeli?”
akutero Yehova.
12 “Koma inu munawamwetsa vinyo anaziri aja,
ndipo munalamula aneneri kuti asanenere.

13 “Tsono Ine ndidzakupsinjani
monga imapsinjikira ngolo imene yadzaza ndi tirigu.
14 Munthu waliwiro sadzatha kuthawa,
munthu wamphamvu sadzakhalanso ndi nyonga,
wankhondo sadzapulumutsa moyo wake.
15 Munthu wa uta sadzalimbika,
msilikali wothamanga kwambiri sadzapulumuka,
ndipo wokwera pa akavalo sadzapulumutsa moyo wake.
16 Ngakhale asilikali olimba mtima kwambiri
adzathawa ali maliseche pa tsikulo,”
akutero Yehova.

# 3

*Mboni Zotsutsa Israeli*

1 Inu Aisraeli, imvani mawu awa amene Yehova wayankhula kutsutsana
nanu, kutsutsana ndi banja lonse limene analitulutsa mu Igupto:
2 “Inu nokha ndi amene ndinakusankhani
pakati pa mabanja onse a dziko lapansi;
n’chifukwa chake ndidzakulangani
chifukwa cha machimo anu onse.”

3 Kodi anthu awiri n’kuyendera limodzi
asanapangane?
4 Kodi mkango umabangula m’nkhalango
usanagwire nyama?
Kodi msona wamkango umalira m’phanga mwake
pamene sunagwire kanthu?
5 Kodi mbalame n’kutera pa msampha
pamene palibe nyambo yake?
Kodi msampha umafwamphuka
usanakole kanthu?
6 Kodi pamene lipenga la nkhondo lalira mu mzinda,
anthu sanjenjemera?
Pamene tsoka lafika mu mzinda,

kodi si Yehova amene wachititsa zimenezo?

7 Zoonadi Ambuye Yehova sachita kanthu
asanawulule zimene akufuna kuchita
kwa atumiki ake, aneneri.

8 Mkango wabangula,
ndani amene sachita mantha?
Ambuye Yehova wayankhula,
ndani amene sanganenere?

9 Lengezani zimenezi ku nyumba zaufumu za ku Asidodi
ndiponso ku nyumba zaufumu za ku Igupto:
"Sonkhanani ku mapiri a ku Samariya;
onani chisokonezo pakati pake
ndiponso kuponderezana pakati pa anthu ake."

10 "Iwo sadziwa kuchita zolungama,
ndipo amadzaza malo awo otetezedwa ndi zinthu zolanda ku nkhondo ndi zakuba," akutero Yehova.
11 N'chifukwa chake Ambuye Yehova akunena izi:
"Mdani adzalizungulira dzikoli;
iye adzagwetsa malinga ako,
ndi kufunkha nyumba zako zaufumu."
12 Yehova akuti,
"Monga m'busa amalanditsa m'kamwa mwa mkango
miyendo iwiri yokha kapena msonga yokha ya khutu,
moteronso ndimo mmene adzapulumukire Aisraeli
amene amakhala mu Samariya
pa msonga za mabedi awo,
ndi ku Damasiko pa akakhutagona awo."
13 "Imvani izi ndipo mupereke umboni wotsutsa nyumba ya Yakobo,"
akutero Ambuye, Yehova Mulungu Wamphamvuzonse.
14 "Pa tsiku limene ndidzalange Israeli chifukwa cha machimo ake,
ndidzagumula maguwa ansembe a ku Beteli;
nyanga za guwa zidzathyoka
ndipo zidzagwa pansi.
15 Ndidzagwetsa nyumba ya pa nthawi yozizira
pamodzi ndi nyumba ya pa nthawi yotentha;
nyumba zokongoletsedwa ndi minyanga ya njovu zidzawonongedwa
ndipo nyumba zikuluzikulu zidzaphwasulidwa,"
akutero Yehova.

# 4

*Israeli Sanabwerere kwa Mulungu*

1 Imvani mawu awa, inu ng'ombe zazikazi za ku Basani, okhala pa Phiri la Samariya,
inu akazi amene mumapondereza anthu osauka ndi kuzunza anthu osowa
ndi kumanena kwa amuna anu kuti, "Tipatseni zakumwa!"
2 Ambuye Yehova, mwa kuyera mtima kwake walumbira kuti,
"Nthawi idzafika ndithu

pamene adzakukokani ndi ngowe,
womaliza wa inu adzakokedwa ndi mbedza.
3 Mudzatulukira m'ming'alu ya pa khoma
aliyense payekhapayekha,
ndipo mudzatayidwa ku Harimoni,"
akutero Yehova.
4 "Bwerani ku Beteli mudzachimwe;
ndi ku Giligala kuti mudzapitirize kuchimwa.
Bweretsani nsembe zanu mmawa uliwonse,
bweretsani chakhumi chanu masiku atatu aliwonse.
5 Wotchani buledi wokhala ndi yisiti ngati nsembe yachiyamiko
ndi kumanyadira poyera za zopereka zanu zaufulu.
Inu Aisraeli, zinyadireni nsembezo,
pakuti izi ndi zimene mumakonda kuchita,"
akutero Ambuye Yehova.

6 "Ndine amene ndinakusendetsani milomo m'mizinda yanu yonse,
ndipo munasowa chakudya m'mizinda yanu.
Komatu inu simunabwerere kwa Ine,"
akutero Yehova.

7 "Ndinenso amene ndinamanga mvula
patangotsala miyezi itatu kuti mukolole.
Ndinagwetsa mvula pa mzinda wina,
koma pa mzinda wina ayi,
mvula inkagwa pa munda wina;
koma sinagwe pa munda wina ndipo mbewu zinawuma.
8 Anthu ankayenda mzinda ndi mzinda kufuna madzi,
koma sanapeze madzi okwanira kumwa.
Komabe inu simunabwerere kwa Ine,"
akutero Yehova.

9 "Nthawi zambiri ndinakantha mbewu zanu ndiponso minda ya mpesa,
ndinayikantha ndi chinsikwi ndiponso ndi chiwawu.
Dzombe linawononga mikuyu yanu ndi mitengo ya olivi.
Komabe inu simunabwerere kwa Ine,"
akutero Yehova.

10 "Ine ndinabweretsa miliri pakati panu
monga ndinachitira ku Igupto.
Ndinapha anyamata anu ndi lupanga,
ndinapereka akavalo anu kwa adani.
Ndinakununkhitsani fungo la mitembo lochokera m'misasa yanu ya nkhondo.
Komatu inu simunabwerere kwa Ine,"
akutero Yehova.

11 "Ndinawononga ena mwa inu
monga ndinawonongera Sodomu ndi Gomora.
Inu munali ngati chikuni choyaka chimene chafumulidwa pa moto.
Komabe inu simunabwerere kwa Ine,"
akutero Yehova.

12 "Choncho izi ndi zimene ndidzakuchitire iwe Israeli,

chifukwa ndidzakuchitira zimenezi,
konzekera kukumana ndi Mulungu wako, iwe Israeli."

13 Iye amene amawumba mapiri,
amalenga mphepo,
ndipo amawululira munthu za m'maganizo ake,
Iye amene amasandutsa usana kuti ukhale mdima,
ndipo amayenda pa zitunda za dziko lapansi,
dzina lake ndi Yehova Mulungu Wamphamvuzonse.

# 5

*Mawu Odandawulira Aisraeli*

1 Israeli, imva mawu awa, nyimbo ya maliro imene ndikuyimba za
iweyo:
2 "Namwali Israeli wagwa,
moti sadzadzukanso,
wasiyidwa m'dziko lake lomwe,
popanda woti ndi kumudzutsa."
3 Ambuye Yehova akuti,
"Mzinda umene udzapite ku nkhondo ndi anthu 1,000 amphamvu
udzatsala ndi anthu 100 okha;
mzinda umene udzapite ku nkhondo ndi anthu 100 amphamvu
udzatsala ndi anthu khumi okha basi."
4 Zimene Yehova akunena kwa nyumba ya Israeli ndi izi:
"Mundifunefune kuti mukhale ndi moyo;
5 musafunefune Beteli,
musapite ku Giligala,
musapite ku Beeriseba.
Pakuti Giligala adzatengedwa ndithu kupita ku ukapolo,
ndipo Beteli adzawonongekeratu."
6 Funani Yehova kuti mukhale ndi moyo,
mukapanda kutero Iye adzatentha nyumba ya Yosefe ngati moto;
motowo udzawononga,
ndipo sipadzakhala wina wozimitsa motowo ku Beteli.

7 Inu amene mumasandutsa chiweruzo cholungama kukhala chowawa
ndi kunyoza chilungamo.
8 (Iye amene analenga nyenyezi za Nsangwe ndi Akamwiniatsatana,
amene amasandutsa mdima kuti ukhale mmawa
ndi kudetsa usana kuti ukhale usiku,
amene amayitana madzi a m'nyanja
ndi kuwathira pa dziko lapansi,
Yehova ndiye dzina lake.
9 Iyeyo amabweretsa chiwonongeko modzidzimutsa pa anthu amphamvu
ndi kuwononga mizinda yotetezedwa),
10 inu mumadana ndi amene amadzudzula m'bwalo la milandu
ndi kunyoza amene amanena zoona.

11 Mumapondereza munthu wosauka
ndi kumukakamiza kuti akupatseni tirigu.
N'chifukwa chake, ngakhale mwamanga nyumba zamiyala yosema,
inuyo simudzakhalamo.

Ngakhale mwalima minda yabwino ya mphesa,
inu simudzamwa vinyo wake.
12 Pakuti Ine ndikudziwa kuchuluka kwa zolakwa zanu
ndi kukula kwa machimo anu.

Inu mumapondereza anthu olungama ndi kulandira ziphuphu
ndipo anthu osauka simuwaweruza mwachilungamo m'mabwalo anu amilandu.
13 N'chifukwa chake pa nthawi yotere munthu wanzeru sayankhulapo kanthu,
popeza ndi nthawi yoyipa.

14 Muyike mtima wanu pa zabwino osati pa zoyipa,
kuti mukhale ndi moyo.
Mukatero Yehova Mulungu Wamphamvuzonse adzakhala nanu,
monga mmene mumanenera kuti ali nanu.
15 Mudane ndi zoyipa, mukonde zabwino;
mukhazikitse chiweruzo cholungama m'mabwalo anu amilandu.
Mwina mwake Yehova Mulungu Wamphamvuzonse adzachitira chifundo
anthu otsala a m'banja la Yosefe.

16 Choncho izi ndi zimene Ambuye, Yehova Mulungu Wamphamvuzonse,
akunena:
"M'misewu monse mudzakhala kulira mofuwula,
ndi kulira chifukwa cha kuwawa kwa masautso kudzakhala paliponse.
Adzayitana alimi kuti adzalire,
ndipo anthu odziwa maliridwe anthetemya adzalira mofuwula.
17 M'minda yonse ya mpesa mudzakhala kulira kokhakokha,
pakuti Ine ndidzadutsa pakati panu,"
akutero Yehova.

### *Tsiku la Yehova*

18 Tsoka kwa inu amene mumalakalaka
tsiku la Yehova!
Chifukwa chiyani mumalakalaka tsiku la Yehova?
Tsikulo kudzakhala mdima osati kuwala.
19 Lidzakhala ngati tsiku limene munthu pothawa mkango
amakumana ndi chimbalangondo,
ngati pamene munthu walowa m'nyumba,
natsamira dzanja lake pa khoma
ndipo njoka n'kuluma.
20 Kodi tsiku la Yehova silidzakhala mdima osati kuwala,
mdima wandiweyani, popanda powala pena paliponse?

21 "Ndimadana nawo masiku anu achikondwerero ndipo ndimawanyoza;
sindikondwera nayo misonkhano yanu.
22 Ngakhale mupereke nsembe zopsereza ndi nsembe zachakudya,
Ine sindidzazilandira.
Ngakhale mupereke nsembe zabwino zachiyanjano,
Ine sindidzaziyang'ana n'komwe.
23 Musandisokose nazo nyimbo zanu!
Sindidzamvetsera kulira kwa azeze anu.
24 Koma chiweruzo cholungama chiyende ngati madzi,
chilungamo ngati mtsinje wosaphwa!

25 “Kodi pa zaka makumi anayi zimene munakhala m’chipululu muja
munkandibweretsera nsembe ndi zopereka, inu nyumba ya Israeli?
26 Inu mwanyamula kachisi wa mfumu yanu,
ndi nyenyezi ija Kaiwani,
mulungu wanu,
mafano amene munadzipangira.
27 N’chifukwa chake Ine ndidzakupititsani ku ukapolo, kutali kupitirira ku Damasiko,”
akutero Yehova, amene dzina lake ndi Mulungu Wamphamvuzonse.

# 6

*Tsoka kwa Osalabadira Kanthu*

1 Tsoka kwa amene simukulabadira kanthu ku Ziyoni,
ndiponso kwa inu amene mukukhala mwamtendere pa Phiri la Samariya,
inu anthu otchuka ochokera ku mtundu wa anthu omveka,
kumene Aisraeli amafikako!
2 Pitani ku mzinda wa Kaline mukawuyang’ane;
mukapitenso ku Hamati-raba mzinda waukulu uja,
ndipo mukatsikirenso ku Gati kwa Afilisti.
Kodi mizinda imeneyi ndi yopambana maufumu anu awiriwa?
Kodi dziko lawo ndi lalikulu kupambana lanu?
3 Inu simulabadirako kuti tsiku loyipa lidzafika,
zochita zanu zimafulumizitsa ulamuliro wankhanza.
4 Mumagona pa mabedi owakongoletsa ndi minyanga ya njovu,
mumagona pa mipando yanu ya wofuwofu.
Mumadya ana ankhosa onona
ndi ana ang’ombe onenepa.
5 Mumayimba azeze anu ndi kumangopeka
nyimbo pa zing’wenyeng’wenye ngati Davide.
6 Mumamwera vinyo m’zipanda zodzaza
ndipo mumadzola mafuta abwino kwambiri,
koma simumva chisoni ndi kuwonongeka kwa Yosefe.
7 N’chifukwa chake inu mudzakhala m’gulu la anthu oyamba kupita ku ukapolo;
maphwando ndi zikondwerero zanu zidzatheratu.

*Yehova Amanyansidwa ndi Kunyada kwa Israeli*

8 Ambuye Yehova walumbira m’dzina lake. Yehova Mulungu
Wamphamvuzonse walengeza kuti,
“Ndimanyansidwa ndi kunyada kwa Yakobo,
ndimadana ndi nyumba zake zaufumu;
Ine ndidzawupereka mzindawu
pamodzi ndi zonse zili m’menemo.”
9 Ngati anthu khumi otsala adzabisala m’nyumba imodzi, nawonso
adzafa ndithu. 10 Ndipo ngati m’bale wake wa wina wakufayo, woyen-
era kusamala za maliro, adzafika kudzatulutsa mitembo m’nyumbamo
n’kufunsa aliyense amene akubisalabe m’nyumbamo kuti, “Kodi uli ndi
wina wamoyo m’menemo?” Ndipo munthu wobisalayo ndi kuyankha kuti,
“Ayi,” m’baleyo adzanena kuti, “Khala chete! Ife tisayerekeze kutchula
dzina la Yehova.”
11 Pakuti Yehova walamula kuti

nyumba zikuluzikulu Iye adzazigamulagamula,
ndipo nyumba zazing'ono zidzasanduka maduka okhaokha.

12 Kodi akavalo amathamanga pa thanthwe?
Kodi wina amatipula ndi ng'ombe m'nyanja?
Koma chiweruzo cholungama mwachisandutsa kukhala zinthu zakupha
ndipo chipatso cha chilungamo mwachisandutsa kukhala chowawa.
13 Inu amene mukunyadira kuti munagonjetsa Lo Debara
ndipo mukunena kuti, "Kodi sitinatenge Karinaimu ndi mphamvu zathu zokha?"

14 Koma Yehova Mulungu Wamphamvuzonse akulengeza kuti,
"Inu nyumba ya Israeli, ndidzakudzutsirani mtundu wina wa anthu umene udzakuzunzani
kuchokera ku Lebo Hamati mpaka ku Chigwa cha Araba."

# 7

### *Dzombe, Moto ndi Chingwe Chowongolera Khoma*

1 Zimene Ambuye Yehova anandionetsa ndi izi: Yehova ankasonkhan-
itsa gulu la dzombe nthawi imene gawo la zokolola za mfumu linali
litakololedwa kale ndipo mbewu zachiwiri zinali zitangoyamba kumera
kumene. 2 Dzombelo litadya zomera zonse za m'dzikomo, Ine ndinafuwula
kuti, "Ambuye Yehova, khululukani! Kodi Yakobo adzapulumuka bwanji?
Iye ndi wofowoka kwambiri!"

3 Kotero Yehova anakhululuka.
Yehovayo anati, "Izi sizidzachitika."

4 Zimene Ambuye Yehova anandionetsa ndi izi: Ambuye Yehova
ankayitana malawi a moto kuti alange anthu. Motowo unawumitsa nyanja
yakuya ndi kupsereza dziko. 5 Tsono ine ndinafuwula kuti, "Ambuye
Yehova, chonde ndikukupemphani, lekani! Kodi Yakobo adzapulumuka
bwanji? Iye ndi wofowoka kwambiri!"

6 Kotero Yehova anakhululuka.
Ambuye Yehova anati, "Izinso sizidzachitika."

7 Zimene Iye anandionetsa ndi izi: Ambuye anayima pambali pa khoma
lomangamanga, m'manja mwake muli chingwe chowongolera khoma.
8 Ndipo Ambuye anandifunsa kuti, "Amosi, n'chiyani ukuonachi?"
Ine ndinayankha kuti, "Chingwe chowongolera khoma."
Ndipo Yehova anati, "Taona, Ine ndikuyika chingwe chowongolerachi pakati pa anthu anga, Aisraeli; sindidzawalekereranso.
9 "Malo achipembedzo a Isake adzawonongedwa
ndipo malo opatulika a Israeli adzasanduka bwinja;
ndidzagwetsa nyumba ya Yeroboamu ndi lupanga langa."

### *Amosi ndi Amaziya*

10 Pamenepo Amaziya wansembe wa ku Beteli anatumiza uthenga kwa
Yeroboamu mfumu ya Israeli kuti, "Amosi akukuutsirani chiwembu pakati
pa Aisraeli. Dziko silingalekerere zonena zake zonsezo. 11 Pakuti zimene
Amosi akunena ndi izi:
" 'Yeroboamu adzaphedwa ndi lupanga,
ndipo Israeli adzapita ndithu ku ukapolo,
kutali ndi dziko lake.' "

12 Ndipo Amaziya anawuza Amosi kuti, “Choka, mlosi iwe! Bwerera
ku dziko la Yuda. Uzikalosera kumeneko ndipo anthu a kumeneko
azikakudyetsa. 13 Usanenerenso ku Beteli, chifukwa kumeneko ndi
malo opatulika a mfumu ndiponso ndi malo a nyumba yachipembedzo
yaufumu.”
14 Amosi anayankha Amaziya kuti, “Ine sindine mneneri kapena
mwana wa mneneri; koma ndine woweta ziweto, ndiponso mlimi wa
nkhuyu. 15 Koma Yehova ananditenga ndikuweta nkhosa ndipo anati, ‘Pita
ukanenere kwa anthu anga Aisraeli.’ 16 Tsono imva mawu a Yehova. Iwe
ukunena kuti,

“ ‘Usanenere zotsutsa Israeli,
ndipo siya kulalikira motsutsa nyumba ya Isake.’ ”

17 “Tsono zimene akunena Yehova ndi izi:

“ ‘Mkazi wako adzasanduka wachiwerewere mu mzindamu,
ndipo ana ako aamuna ndi aakazi adzaphedwa ndi lupanga.
Munda wako udzayezedwa ndi chingwe ndi kugawidwa,
ndipo iwe mwini udzafera m’dziko la anthu osapembedza Mulungu.
Ndipo Israeli adzatengedwa ndithu kupita ku ukapolo,
kutali ndi dziko lake.’ ”

# 8

*Dengu la Zipatso Zakupsa*

1 Zimene Ambuye Yehova anandionetsa ndi izi: dengu la zipatso
zakupsa. 2 Iye anandifunsa kuti, “Amosi n’chiyani ukuona?”

Ine ndinayankha kuti, “Dengu la zipatso zakupsa.”

Ndipo Yehova anati kwa ine, “Nthawi yachimaliziro yawakwanira anthu anga Aisraeli; sindidzawakhululukiranso.

3 “Tsiku limenelo,” Ambuye Yehova akulengeza kuti, “Nyimbo za
m’Nyumba ya Mulungu zidzasanduka kulira kofuwula. Mitembo ya anthu
idzachuluka, ndipo adzayiponya ponseponse! Kudzangoti zii!”

4 Imvani izi, inu amene mumapondereza anthu osowa
ndipo simulabadira anthu osauka a m’dzikomu.

5 Mumanena kuti,

“Kodi chikondwerero cha mwezi watsopano chidzatha liti
kuti tigulitse zinthu?
Ndipo tsiku la Sabata litha liti
kuti tigulitse tirigu,
kuti tichepetse miyeso,
kukweza mitengo
kuti tibere anthu ndi miyeso ya chinyengo,
6 tigule osauka ndi ndalama zasiliva
ndi osowa powapatsa nsapato,
tigulitse ngakhale mungu wa tirigu?”

7 Yehova amene Yakobo amamunyadira, walumbira kuti: Ine sindidza-
yiwala chilichonse chimene anachita.

8 “Kodi dziko silidzagwedezeka chifukwa cha zimenezi,
ndi onse okhala m’menemo kulira mwachisoni?
Dziko lonse lidzavunduka ngati mtsinje wa Nailo;
lidzagwedezeka kenaka n’kukhala bata
ngati mtsinje wa ku Igupto.

9 “Tsiku limenelo,” Ambuye Yehova akunena kuti,

“Ndidzadetsa dzuwa masana

ndi kugwetsa mdima pa dziko lapansi dzuwa likuswa mtengo.
10 Maphwando anu achipembedzo ndidzawasandutsa kulira kwa chisoni
ndipo kuyimba kwanu konse ndidzakusandutsa maliro.
Ndidzakuvekani chiguduli nonsenu
ndi kumeta mipala mitu yanu.
Nthawi imeneyo idzakhala ngati yolira mwana wamwamuna mmodzi yekhayo,
ndipo tsikulo lidzakhala lowawa mpaka kutha kwake.

11 “Nthawi ikubwera,” Ambuye Yehova akunena kuti,
“Ndidzagwetsa njala m’dziko lonse;
osati njala ya chakudya kapena ludzu la madzi,
koma njala yofuna kumva mawu a Yehova.
12 Anthu azidzangoyendayenda kuchoka ku nyanja ina kupita ku nyanja ina.
Azidzangoyendayenda kuchoka kumpoto kupita kummawa,
kufunafuna mawu a Yehova,
koma sadzawapeza.
13 “Tsiku limenelo
“anamwali okongola ndi anyamata amphamvu
adzakomoka ndi ludzu.
14 Onse amene amalumbira pa tchimo la Samariya,
kapena kumanena kuti, ‘Iwe Dani, pali mulungu wako wamoyo,’
kapena, ‘Pali mulungu wamoyo wa ku Beeriseba.’
Iwowo adzagwa
ndipo sadzadzukanso.”

# 9

*Israeli Adzawonongedwa*

1 Ine ndinaona Ambuye atayima pambali pa guwa lansembe, ndipo anati:
“Kantha mitu ya nsanamira
kuti ziwundo za nyumba zigwedezeke.
Muzigwetsere pa mitu ya anthu onse,
onse amene atsalira ndidzawapha ndi lupanga.
Palibe ndi mmodzi yemwe amene adzathawe,
palibe amene adzapulumuke.
2 Ngakhale atakumba pansi mpaka ku malo a anthu akufa,
dzanja langa lidzawatulutsa kumeneko.
Ngakhale atakwera kumwamba
Ine ndidzawatsakamutsa kumeneko.
3 Ngakhale atakabisala pamwamba pa phiri la Karimeli,
Ine ndidzawasaka kumeneko ndi kuwagwira.
Ngakhale atakabisala pansi pa nyanja yayikulu,
ndidzalamula njoka kuti iwalume kumeneko.
4 Ngakhale adani awo awakusire ku ukapolo,
ndidzalamula lupanga kuti liwaphe kumeneko.
Ndidzawayang’anitsitsa
kuti zoyipa ziwagwere; osati zabwino.”

5 Ambuye Yehova Wamphamvuzonse
amene amakhudza dziko lapansi ndipo dzikolo limasungunuka,
onse amene amakhala m’menemo amalira.

Dziko lonse lidzadzaza ngati mtsinje wa Nailo,
kenaka n'kuphwera ngati mtsinje wa ku Igupto.
6 Iye amene amamanga malo ake okhalamo kumwamba,
ndi kuyika maziko ake pa dziko lapansi,
Iye amene amayitana madzi a ku nyanja
ndikuwakhuthulira pa dziko lapansi,
dzina lake ndiye Yehova.

7 "Kodi kwa Ine, inu Aisraeli, simuli
chimodzimodzi ndi Akusi?"
Akutero Yehova.
"Kodi sindine amene ndinatulutsa Israeli ku Igupto,
Afilisti ku Kafitori
ndi Aaramu ku Kiri?

8 "Taonani, maso a Ambuye Yehova
ali pa ufumu wochimwawu.
Ndidzawufafaniza
pa dziko lapansi.
Komabe sindidzawononga kotheratu
nyumba ya Yakobo,"
akutero Yehova.
9 "Pakuti ndidzalamula,
ndipo ndidzagwedeza nyumba ya Israeli
pakati pa mitundu yonse ya anthu
monga momwe amasefera ufa m'sefa,
koma palibe n'kamwala kamodzi komwe kamene kadzagwe pansi.
10 Anthu onse ochimwa pakati pa anthu anga
adzaphedwa ndi lupanga,
onse amene amanena kuti,
'Tsoka silidzatigwera ife kapena kutiwononga.'

### *Kubwezeretsedwa kwa Israeli*

11 "Tsiku limenelo ndidzabwezeretsa
nyumba ya Davide imene inagwa.
Ndidzakonzanso malo amene anagumuka,
ndi kuyimanganso
monga inalili poyamba,
12 kuti adzatengenso otsala a Edomu
ndi mitundu yonse imene imatchedwa ndi dzina langa,"
akutero Yehova amene adzachita zinthu izi.
13 Yehova akunena kuti
"Nthawi ikubwera pamene mlimi wotipula adzapyola wokolola
ndipo woponda mphesa adzapyola wodzala mbewu.
Mapiri adzachucha vinyo watsopano
ndi kuyenderera pa zitunda zonse.
14 Ndidzawabwezeranso pabwino anthu anga Aisraeli;
mizinda imene inali mabwinja idzamangidwanso ndipo azidzakhalamo.
Adzalima minda ya mpesa ndipo adzamwa vinyo wake;
adzalima minda ndipo adzadya zipatso zake.
15 Ndidzakhazika Aisraeli m'dziko mwawo,
ndipo sadzachotsedwamonso m'dziko
limene Ine ndawapatsa,"

akutero Yehova Mulungu wako.

# Obadiya

*Masomphenya a Obadiya*

1 Masomphenya a Obadiya.

Ambuye Yehova akunena kwa Edomu kuti,
Tamva uthenga wochokera kwa Yehova:
Nthumwi yatumidwa kupita kwa anthu a mitundu kukanena kuti,
"Konzekani, tiyeni tikachite nkhondo ndi Edomu."

2 "Taona, ndidzakuchepetsani pakati pa anthu a mitundu ina;
udzanyozedwa kwambiri.
3 Kudzikuza kwa mtima wako kwakusocheretsa,
iwe amene umakhala m'mapanga a m'matanthwe
ndipo umamanga nyumba zako pa mapiri ataliatali,
iwe amene umanena mu mtima mwako kuti,
'Ndani anganditsitse pansi?'
4 Koma ngakhale umawuluka ngati chiwombankhanga
ndi kumanga chisa chako pakati pa nyenyezi,
ndidzakutsitsa pansi kuchokera kumeneko,"
akutero Yehova.
5 "Anthu akuba akanabwera kwa iwe,
kapena anthu olanda zinthu akanafika usiku,
aa, tsoka lanji limene likukudikira iwe!
Kodi akanangotengako zimene akuzifuna zokha?
Ngati anthu othyola mphesa akanafika,
kodi akanakusiyiraniko mphesa pang'ono pokha?
6 Koma Esau adzalandidwa zinthu zonse,
chuma chake chobisika chidzabedwa!
7 Anthu onse ogwirizana nawo adzakupirikitsira kumalire;
abwenzi ako adzakunyenga ndi kukugonjetsa;
amene amadya chakudya chako adzakutchera msampha,
koma iwe sudzazindikira zimenezi."

8 Yehova akunena kuti, "Tsiku limenelo,
kodi sindidzawononga anthu onse anzeru a ku Edomu,
anthu odziwa zinthu m'mapiri a Esau?
9 Ankhondo ako, iwe Temani, adzachita mantha,
ndipo aliyense amene ali m'phiri la Esau
adzaphedwa pa nkhondo.
10 Chifukwa cha nkhanza zimene unachitira m'bale wako Yakobo,
udzakhala wamanyazi;
adzakuwononga mpaka muyaya.
11 Pamene adani
ankamulanda chuma chake
pamene alendo analowa pa zipata zake
ndi kuchita maere pa Yerusalemu,
pa tsikulo iwe unali ngati mmodzi wa iwo.
12 Iwe sunayenera kunyoza m'bale wako
pa nthawi ya tsoka lake,

kapena kunyogodola Ayuda
chifukwa cha chiwonongeko chawo,
kapena kuwaseka pa nthawi ya
mavuto awo.
13 Iwe sunayenera kudutsa pa zipata za anthu anga
pa nthawi ya masautso awo,
kapena kuwanyogodola
pa tsiku la tsoka lawo,
kapena kulanda chuma chawo
pa nthawi ya masautso awo.
14 Sunayenera kudikirira pamphambano ya misewu
kuti uphe Ayuda othawa,
kapena kuwapereka kwa adani awo Ayuda opulumuka
pa nthawi ya mavuto awo."

15 "Tsiku la Yehova layandikira
limene adzaweruza mitundu yonse ya anthu.
Adzakuchitira zomwe unawachitira ena;
zochita zako zidzakubwerera wekha.
16 Iwe unamwa pa phiri langa loyera,
koteronso mitundu ina yonse idzamwa kosalekeza;
iwo adzamwa ndi kudzandira
ndipo adzayiwalika pa mbiri ya dziko lapansi.
17 Koma pa Phiri la Ziyoni padzakhala chipulumutso;
phirilo lidzakhala lopatulika,
ndipo nyumba ya Yakobo
idzalandira cholowa chake.
18 Nyumba ya Yakobo idzasanduka moto
ndipo nyumba ya Yosefe idzasanduka lawi la moto;
nyumba ya Esau idzasanduka chiputu,
ndipo adzayitenthe pa moto ndi kuyipsereza.
Sipadzakhala anthu opulumuka
kuchokera m'nyumba ya Esau."
Yehova wayankhula.

19 Anthu ochokera ku Negevi adzakhala
ku mapiri a Esau,
ndipo anthu ochokera m'mbali mwa mapiri
adzatenga dziko la Afilisti.
Adzakhala m'minda ya Efereimu ndi Samariya,
ndipo Benjamini adzatenga Giliyadi.
20 Aisraeli amene ali ku ukapolo
adzalandira dziko la Kanaani mpaka ku Zarefati;
a ku Yerusalemu amene ali ku ukapolo ku Sefaradi
adzalandira mizinda ya ku Negevi.
21 Opulumukawo adzapita ku Phiri la Ziyoni
ndipo adzalamulira mapiri a Esau.
Koma ufumuwo udzakhala wa Yehova.

# Yona

*Yona Athawa Yehova*

1 Yehova anayankhula ndi Yona mwana wa Amitai kuti, 2 "Nyamuka,
pita ku mzinda waukulu wa Ninive ndipo ukalalikire motsutsana nawo,
chifukwa zoyipa zawo zafika pamaso panga."

3 Koma Yona anathawa Yehova ndi kulowera ku Tarisisi. Anapita ku
Yopa, kumene anapeza sitima yapamadzi yopita ku Tarisisi. Atagula
chiphaso, anakwera sitimayo kupita ku Tarisisi kuthawa Yehova.

4 Koma Yehova anatumiza chimphepo champhamvu pa nyanja, ndipo
panauka namondwe wamphamvu amene anafuna kuphwanya sitimayo.

5 Onse oyendetsa sitimayo anachita mantha ndipo aliyense anayamba
kupemphera kwa mulungu wake. Ndipo anaponya katundu m'nyanja kuti
sitimayo ipepuke. Koma Yona pa nthawiyi n'kuti atatsikira m'katikati
mwa sitimayo kumene anagona tulo tofa nato. 6 Mkulu wa oyendetsa
sitimayo anapita kwa iye ndipo anati, "Kodi iwe, n'chifukwa chiyani
ukugona? Dzuka pemphera kwa mulungu wako! Mwina adzatithandiza,
ndipo sitidzawonongeka."

7 Ndipo oyendetsa sitimayo anayamba kuwuzana kuti, "Bwerani, tichite
maere kuti tipeze amene wabweretsa tsoka limeneli." Iwo anachita
maerewo ndipo anagwera Yona.

8 Tsono anamufunsa kuti, "Tatiwuze, tsoka limeneli latigwera chifukwa
chiyani? Umagwira ntchito yanji? Ukuchokera kuti? Kwanu n'kuti?
Ndiwe mtundu wanji wa anthu?"

9 Iye anayankha kuti, "Ndine Mhebri, ndipo ndimapembedza Yehova,
Mulungu Wakumwamba, amene analenga nyanja ndi mtunda."

10 Izi zinawachititsa mantha kwambiri ndipo anafunsa kuti, "Kodi
wachita chiyani?" (Iwo ankadziwa kuti iyeyo amathawa Yehova, chifukwa
n'kuti atawawuza kale).

11 Namondwe ananka nakulirakulirabe pa nyanjapo. Tsono anamufunsa
iye kuti, "Kodi tikuchite chiyani kuti nyanjayi ikhale bata?"

12 Iye anayankha kuti, "Nyamuleni ndi kundiponya m'nyanjamu ndipo
nyanjayi ikhala bata. Ndikudziwa kuti wolakwa ndine n'chifukwa chake
chimphepo champhamvuchi chabwera pa inu."

13 Komabe oyendetsa sitimayo anayesetsa kupalasa kwambiri kuti
abwerere ku mtunda koma analephera ndithu poti nyanja inawinduka
kwambiri kuposa poyamba paja 14 Pamenepo iwo anafuwulira kwa Yehova
nati, "Inu Yehova, musalole kuti ife tife chifukwa cha moyo wa munthu
uyu. Musatizenge mlandu wa kupha munthu wosalakwa, pakuti ife
tachita monga mwakufuna kwanu, Inu Yehova." 15 Ndipo anatenga
Yona namuponya m'nyanja, ndipo nyanja yowindukayo inakhala bata.
16 Anthuwo ataona zimenezi anachita mantha akulu ndi Yehova, ndipo
anapereka nsembe kwa Yehova nalumbira kuti adzatumikira Yehovayo.

17 Koma Yehova anatuma nsomba yayikulu kuti imeze Yona. Motero
Yona anakhala m'mimba mwa nsombayo masiku atatu, usana ndi usiku.

## 2

*Pemphero la Yona*

[1] Yona ali m'mimba mwa chinsomba chija anapemphera kwa Yehova
Mulungu wake. [2] Iye anati:
"Pamene ndinali m'mavuto anga ndinayitana Yehova,
ndipo Iye anandiyankha.
Ndili ku dziko la anthu akufa ndinapempha thandizo,
ndipo Inu munamva kulira kwanga.
[3] Munandiponya m'nyanja yozama,
m'kati mwenimweni mwa nyanja,
ndipo madzi oyenda anandizungulira;
mafunde anu onse ndi mkokomo wake
zinandimiza.
[4] Ndinati, 'Ine ndachotsedwa
pamaso panu;
komabe ndidzayang'ananso
ku Nyumba yanu yopatulika.'
[5] Madzi wondimiza anandichititsa mantha,
nyanja yozama inandizungulira;
udzu wa m'madzi zinakuta mutu wanga.
[6] Ndinatsikira kunsi ndithu, m'tsinde mwa mapiri;
mipiringidzo ya dziko inanditsekereza kosatha.
Koma Inu munatulutsa moyo wanga m'mandamo,
Inu Yehova Mulungu wanga.

[7] "Pamene moyo wanga umachoka mwa ine,
ine ndinakumbukira Inu Yehova,
ndipo pemphero langa linafika kwa inu,
ku Nyumba yanu yopatulika.

[8] "Iwo amene amagwiritsitsa mafano achabechabe
amataya chisomo chawo.
[9] Koma ine ndidzapereka kwa Inu nsembe
ndikuyimba nyimbo yamayamiko.
Chimene ndinalonjeza ndidzachikwaniritsa.
Chipulumutso chimachokera kwa Yehova."
[10] Ndipo Yehova analamula chinsomba chija, ndipo chinakamusanza
Yonayo m'mbali mwa nyanja.

# 3

*Yona Apita ku Ninive*

[1] Ndipo Yehova anayankhula ndi Yona kachiwiri kuti, [2] "Nyamuka,
pita ku mzinda waukulu wa Ninive ndipo ukalalikire uthenga umene
ndikupatsa."
[3] Yona anamvera mawu a Yehova ndipo anapita ku Ninive. Tsono
Ninive unali mzinda waukulu kwambiri; wofunika masiku atatu
kuwudutsa. [4] Yona analowa mu mzindawo, nayenda ulendo wa tsiku
limodzi. Iye ankalalikira kuti, "Atsala masiku makumi anayi kuti
Ninive awonongedwe." [5] Anthu a ku Ninive anakhulupirira Mulungu.
Analengeza kuti aliyense, wamkulu ndi wamng'ono yemwe asale zakudya
ndipo avale chiguduli.
[6] Mfumu ya ku Ninive itamva nkhaniyi, inatsika pa mpando wake
waufumu, nivula mkanjo wake waufumu ndipo inavala chiguduli ndi
kukhala pansi pa fumbi. [7] Tsono mfumuyo inalengeza mu Ninive kuti,

"Mwa lamulo lochokera kwa mfumu ndi akalonga ake:

"Munthu aliyense kapenanso nyama, ng'ombe kapena nkhosa,
zisadye kanthu kalikonse; musazilole kuti zidye kapena kumwa. [8] Koma
anthu avale ziguduli, ndipo nyamanso aziveke ziguduli. Munthu
aliyense azifuwula kwa Mulungu ndi mphamvu zake zonse. Anthuwo
asiye makhalidwe awo oyipa ndi machitidwe achiwawa. [9] Angadziwe
ndani? Mwina Mulungu n'kutikhululukira ndipo mwa chifundo chake
n'kuleka kutikwiyira, ifeyo osawonongedwa."

[10] Mulungu ataona zimene anthuwo anachita, ndi mmene anasiyira
makhalidwe awo oyipa, anawachitira chifundo ndipo sanabweretse chi-
wonongeko chimene anawaopseza nacho.

# 4

*Mkwiyo wa Yona ndi Chifundo cha Yehova*

[1] Koma Yona anakhumudwa kwambiri ndipo anakwiya. [2] Iye anapem-
phera kwa Yehova kuti, "Inu Yehova, kodi izi si zimene ndinanena
ndikanali kwathu? N'chifukwa chaketu ine ndinafulumira kuthawa
kupita ku Tarisisi. Ine ndinadziwa kuti ndinu Mulungu wokoma mtima
ndi wachifundo, wosakwiya msanga ndi wa chikondi chopanda malire,
Mulungu amene mumaleka kubweretsa tsoka. [3] Ndipo tsopano, Inu
Yehova, ingondiphani basi, pakuti ndi bwino kuti ndife kupambana
n'kukhala ndi moyo."

[4] Koma Yehova anayankha kuti, "Kodi n'koyenera kuti iwe ukwiye?"

[5] Yona anatuluka mu mzindamo nakakhala pansi cha kummawa kwa
mzindawo. Kumeneko anadzimangira chithando nakhala m'menemo mu
mthunzi, kudikira kuti aone zimene zichitikire mzindawo. [6] Tsono Yehova
Mulungu anameretsa msatsi ndi kuyikulitsa kuti ipereke mthunzi kwa
Yona kuchotsa mavuto ake; ndipo Yona anasangalala kwambiri chifukwa
cha msatsiyo. [7] Koma tsiku linalo mmawa, Mulungu anabweretsa mbozi
imene inadya msatsiyo ndipo inafota. [8] Dzuwa litatuluka, Yehova anab-
weretsa mphepo yotentha yochokera kummawa, ndipo dzuwa linatentha
pamutu pa Yona kotero analenguka nalo. Iye anangofuna atafa, ndipo
anati, "Ndi bwino kuti ndife kupambana n'kukhala ndi moyo."

[9] Koma Mulungu anati kwa Yona, "Kodi n'koyenera kuti iwe ukwiye
chifukwa cha msatsi?"

Iye anayankha kuti, "Inde n'koyenera. Kukwiya kwanga n'kofuna kufa
nako."

[10] Koma Yehova anati, "Iwe ukumvera chisoni msatsiwo, ngakhale kuti
sunawugwirire ntchito kapena kuwukulitsa. Inamera pa usiku umodzi
ndipo inafanso pa usiku umodzi. [11] Koma mu Ninive muli anthu opitirira
120,000 amene sadziwa kusiyanitsa kuti chabwino n'chiti ndipo choyipa
n'chiti, mulinso ziweto zochuluka. Kodi sindiyenera kumvera chisoni
mzinda waukulu ngati uwu?"

# Mika

1 Yehova anayankhula ndi Mika wa ku Moreseti pa nthawi ya ulamuliro
wa Yotamu, Ahazi ndi Hezekiya, mafumu a ku Yuda. Awa ndi masom-
phenya amene iye anaona onena za Samariya ndi Yerusalemu.
2 Tamverani, inu anthu a mitundu yonse,
mvetsera iwe dziko lapansi ndi okhala m'menemo,
pakuti Ambuye Yehova achitira umboni wokutsutsani,
Ambuye akuyankhula ali m'nyumba yake yopatulika.

*Chiweruzo cha Samariya ndi Yerusalemu*

3 Taonani! Yehova akubwera kuchokera ku malo ake;
Iye akutsika ndipo akuponda pa malo okwera a dziko lapansi.
4 Mapiri akusungunuka pansi pake,
ndipo zigwa zikugawikana
ngati phula pa moto,
ngati madzi ochokera m'phiri.
5 Zonsezi ndi chifukwa cha cholakwa cha Yakobo,
chifukwa cha machimo a nyumba ya Israeli.
Kodi cholakwa cha Yakobo n'chiyani?
Kodi si Samariya?
Kodi malo achipembedzo a Yuda ndi ati?
Kodi si Yerusalemu?

6 "Choncho Ine ndidzasandutsa Samariya kukhala bwinja,
malo odzalamo mphesa.
Miyala yake ndidzayitaya ku chigwa
ndipo ndidzafukula maziko ake.
7 Mafano ake onse ndidzawaphwanyaphwanya;
mphatso zake zonse ndidzazitentha ndi moto;
ndidzawononga zifanizo zonse za milungu yake.
Popeza analandira mphatso zake kuchokera ku malipiro a akazi achiwerewere,
mphatsozonso zidzagwiritsidwa ntchito ndi ena ngati malipiro a akazi achiwerewere."

*Kulira ndi Kumva Chisoni*

8 Chifukwa cha zimenezi ine ndidzalira momvetsa chisoni;
ndidzayenda wopanda nsapato ndi wamaliseche.
Ndidzafuwula ngati nkhandwe
ndi kulira ngati kadzidzi.
9 Pakuti chilonda cha Samariya n'chosachizika;
chafika ku Yuda.
Chafika pa chipata chenicheni cha anthu anga,
mpaka mu Yerusalemu mwenimwenimo.
10 Musanene zimenezi ku Gati;
musalire n'komwe.
Mugubuduzike mu fumbi
ku Beti-Leafura.
11 Inu anthu okhala ku Safiro,
muzipita ku ukapolo muli amaliseche ndi amanyazi.
Iwo amene akukhala ku Zanaani

sadzatuluka.
Beti-Ezeli akulira mwachisoni;
chitetezo chake chakuchokerani.
12 Anthu amene amakhala ku Maroti akubuwula ndi ululu,
akuyembekezera thandizo,
chifukwa Yehova wabweretsa tsoka,
lafika mpaka pa chipata cha Yerusalemu.
13 Inu anthu okhala ku Lakisi
mangani akavalo ku magaleta.
Inu amene munayamba kuchimwitsa
mwana wamkazi wa Ziyoni,
pakuti zolakwa za Israeli
zinapezeka pakati panu.
14 Chifukwa chake perekani mphatso zolawirana
ndi a ku Moreseti Gati.
Mzinda wa Akizibu udzaonetsa kunama
kwa mafumu a Israeli.
15 Ndidzabweretsa mgonjetsi kudzalimbana ndi inu
okhala mu Maresa.
Ulemerero wa Israeli udzafika
ku Adulamu.
16 Metani mipala mitu yanu kuonetsa kuti mukulirira
ana anu amene mumawakonda;
mudzichititse dazi ngati dembo,
pakuti anawo adzatengedwa pakati panu kupita ku ukapolo.

# 2

### *Zokonzekera za Munthu ndi Zokonzekera za Mulungu*

1 Tsoka kwa amene amakonzekera chiwembu,
kwa amene amakonzekera kuchita zoyipa usiku pa mabedi awo!
Kukacha mmawa amakachitadi
chifukwa ali ndi mphamvu zochitira zimenezo.
2 Amasirira minda ndi kuyilanda,
amasirira nyumba ndi kuzilanda.
Amatenga nyumba ya munthu mwachinyengo,
munthu mnzawo kumulanda cholowa chake.
3 N'chifukwa chake Yehova akuti,
"Ine ndikukonzekera kubweretsa tsoka pa anthu awa,
tsoka limene simudzatha kudzipulumutsa nokha.
Inu simudzayendanso monyada,
pakuti idzakhala nthawi ya masautso.
4 Tsiku limenelo anthu adzakuchitani chipongwe;
adzakunyogodolani ndi nyimbo iyi yamaliro:
'Tawonongeka kotheratu;
dziko la anthu anga lagawidwa.
Iye wandilanda!
Wapereka minda yathu kwa anthu otiwukira.' "

5 N'chifukwa chake simudzakhala ndi munthu mu msonkhano wa Yehova
kuti agawe dziko pochita maere.

### *Aneneri Onyenga*

6 Aneneri awo amanena kuti, "Usanenere!

Usanenere ndi pang'ono pomwe zimenezi;
ife sitidzachititsidwa manyazi."
7 Inu nyumba ya Yakobo, monga zimenezi ndi zoyenera kuzinena:
"Kodi Mzimu wa Yehova wakwiya?
Kodi Iye amachita zinthu zotere?"

"Kodi mawu ake sabweretsa zabwino
kwa amene amayenda molungama?
8 Posachedwapa anthu anga andiwukira
ngati mdani.
Mumawavula mkanjo wamtengowapatali
anthu amene amadutsa mosaopa kanthu,
monga anthu amene akubwera ku nkhondo.
9 Mumatulutsa akazi a anthu anga
m'nyumba zawo zabwino.
Mumalanda ana awo madalitso anga
kosatha.
10 Nyamukani, chokani!
Pakuti ano si malo anu opumulirapo,
chifukwa ayipitsidwa,
awonongedwa, sangatheke kuwakonzanso.
11 Ngati munthu wabodza ndi wachinyengo abwera n'kunena kuti,
'Ine ndidzanenera ndipo mudzakhala ndi vinyo ndi mowa wambiri,
woteroyo adzakhala mneneri amene anthu awa angamukonde!'

*Alonjeza Chipulumutso*

12 "Inu banja la Yakobo, ndidzakusonkhanitsani nonse;
ndidzawasonkhanitsa pamodzi otsala a ku Israeli.
Ndidzawabweretsa pamodzi ngati nkhosa m'khola,
ngati ziweto pa msipu wake;
malowo adzadzaza ndi chinamtindi cha anthu.
13 Amene adzawapulumutse adzayenda patsogolo pawo;
iwo adzathyola chipata ndipo adzatuluka.
Mfumu yawo idzawatsogolera,
Yehova adzakhala patsogolo pawo."

# 3

*Atsogoleri ndi Aneneri Adzudzulidwa*

1 Ndipo ine ndinati,
"Tamverani, inu atsogoleri a Yakobo,
inu olamulira nyumba ya Israeli.
Kodi sindinu oyenera kudziwa kuweruza molungama,
2 inu amene mumadana ndi zabwino ndi kukonda zoyipa;
inu amene mumasenda khungu la anthu anga,
ndipo mumakungunula mnofu pa mafupa awo;
3 inu amene mumadya anthu anga,
mumasenda khungu lawo
ndi kuphwanya mafupa awo;
inu amene mumawadula nthulinthuli
ngati nyama yokaphika?"

4 Pamenepo adzalira kwa Yehova,

koma Iye sadzawayankha.
Nthawi imeneyo Iye adzawabisira nkhope yake
chifukwa cha zoyipa zimene anazichita.
5 Yehova akuti,
“Aneneri amene
amasocheretsa anthu anga,
ngati munthu wina awapatsa chakudya
amamufunira ‘mtendere;’
ngati munthu wina sawapatsa zakudya
amamulosera zoyipa.
6 N’chifukwa chake kudzakuderani,
simudzaonanso masomphenya,
mdima udzakugwerani ndipo simudzawombezanso.
Dzuwa lidzawalowera aneneriwo, ndipo mdima udzawagwera.
7 Alosi adzachita manyazi
ndipo owombeza mawula adzanyazitsidwa.
Onse adzaphimba nkhope zawo
chifukwa Mulungu sakuwayankha.”

8 Koma kunena za ine, ndadzazidwa ndi mphamvu,
ndi Mzimu wa Yehova,
ndi kulungama, ndi kulimba mtima,
kuti ndilalikire za kugalukira kwa Yakobo,
kwa Israeli za tchimo lake.
9 Imvani izi, inu atsogoleri a nyumba ya Yakobo,
inu olamulira nyumba ya Israeli,
inu amene mumadana ndi kuweruza kolungama;
ndipo mumakhotetsa zinthu zonse zolondola;
10 inu amene mukumanga Ziyoni pokhetsa magazi,
ndi Yerusalemu ndi kuyipa kwanu.
11 Atsogoleri ake amalandira chiphuphu kuti aweruze,
ansembe ake amalandira malipiro kuti alalikire,
ndipo aneneri ake amanenera kuti alandire ndalama.
Komatu amatsamira pa Yehova n’kumanena kuti,
“Kodi Yehova sali pakati pathu?
Palibe tsoka limene lidzatigwere.”
12 Choncho chifukwa cha inu,
Ziyoni adzatipulidwa ngati munda,
Yerusalemu adzasanduka bwinja,
ndipo phiri la Nyumba ya Mulungu lidzasanduka nkhalango yowirira.

# 4

*Phiri la Yehova*

1 M’masiku otsiriza,
phiri la Nyumba ya Yehova adzalikhazikitsa
kukhala lalitali kuposa mapiri ena onse.
Lidzaonekera pamwamba pa mapiri ena onse,
ndipo anthu amitundu yonse adzathamangira kumeneko.
2 Mayiko ambiri adzabwera ndikunena kuti,
“Tiyeni, tikwere ku phiri la Yehova,
ku nyumba ya Mulungu wa Yakobo.
Iye adzatiphunzitsa njira zake,

ndipo tidzayenda m’njira zakezo.”
Malangizo adzachokera ku Ziyoni,
mawu a Yehova adzachokera ku Yerusalemu.
3 Iye adzaweruza pakati pa anthu amitundu yambiri
ndipo adzathetsa kusamvana pakati pa anthu amphamvu akutali ndi apafupi omwe.
Anthuwo adzasandutsa malupanga awo kukhala makasu
ndiponso mikondo yawo kukhala zomwetera.
Mtundu wina sudzatenganso lupanga kumenyana ndi mtundu wina,
kapena kuphunziranso za nkhondo.
4 Munthu aliyense adzakhala pansi pa tsinde pa mtengo wake wa mpesa
ndi pa tsinde pa mtengo wake wamkuyu,
ndipo palibe amene adzawachititse mantha,
pakuti Yehova Wamphamvuzonse wayankhula.
5 Mitundu yonse ya anthu
itha kutsatira milungu yawo;
ife tidzayenda m’njira za Yehova
Mulungu wathu mpaka muyaya.

*Cholinga cha Yehova*

6 “Tsiku limenelo, Yehova akuti,
“ndidzasonkhanitsa olumala;
ndidzasonkhanitsa pamodzi anthu ochotsedwa
ndiponso amene ndinawalanga.
7 Anthu olumalawo ndidzawasandutsa anthu anga otsala.
Anthu amene ndinawachotsa ndidzawasandutsa mtundu wamphamvu.
Yehova adzawalamulira m’Phiri la Yehova
kuyambira tsiku limenelo mpaka muyaya.
8 Kunena za iwe, nsanja ya ziweto zanga,
iwe linga la mwana wamkazi wa Ziyoni,
ulamuliro wako wakale udzabwezeretsedwa kwa iwe;
ufumu udzabwera pa mwana wamkazi wa Yerusalemu.”

9 Chifukwa chiyani tsopano ukulira mofuwula,
kodi ulibe mfumu?
Kodi phungu wako wawonongedwa,
kotero kuti ululu wako uli ngati wa mayi amene akubereka?
10 Gubuduka ndi ululu, iwe mwana wamkazi wa Ziyoni,
ngati mayi pa nthawi yake yobereka,
pakuti tsopano muyenera kuchoka mu mzinda
ndi kugona kunja kwa mzindawo.
Udzapita ku Babuloni;
kumeneko udzapulumutsidwa,
kumeneko Yehova adzakuwombola
m’manja mwa adani ako.

11 Koma tsopano mitundu yambiri ya anthu
yasonkhana kulimbana nawe.
Iwo akuti, “Tiyeni timudetse,
maso athu aone chiwonongeko cha Ziyoni!”
12 Koma iwo sakudziwa
maganizo a Yehova;

iwo sakuzindikira cholinga chake,
Iye amene amawatuta ngati mitolo ya tirigu ku malo opunthira tirigu.

13 “Imirira, puntha, iwe mwana wamkazi wa Ziyoni,
pakuti ndidzakupatsa nyanga zachitsulo;
ndidzakupatsa ziboda zamkuwa
ndipo udzaphwanya mitundu yambiri ya anthu.”

Phindu lawo lolipeza molakwikalo udzalipereka kwa Yehova,
chuma chawo kwa Yehova wa dziko lonse lapansi.

# 5

*Wolamulira Wochokera ku Betelehemu*

1 Iwe mzinda wa anthu ankhondo, sonkhanitsa anthu ako ankhondo,
pakuti anthu atizungulira kuti alimbane nafe.
Adzakantha ndi ndodo pa chibwano
cha wolamulira wa Israeli.

2 “Koma iwe Betelehemu Efurata,
ngakhale uli wonyozeka pakati pa mafuko a Yuda,
mwa iwe mudzatuluka
munthu amene adzalamulira Israeli,
amene chiyambi chake n’chakalekale,
n’chamasiku amakedzana.”

3 N’chifukwa chake Israeli adzasiyidwa
mpaka pa nthawi imene mayi amene ali woyembekezera adzachire.
Ndipo abale ake onse otsalira adzabwerera
kudzakhala pamodzi ndi Aisraeli.

4 Iye adzalimbika, ndipo adzaweta nkhosa zake
mwa mphamvu ya Yehova,
mu ulemerero wa dzina la Yehova Mulungu wake.
Ndipo iwo adzakhala mu mtendere,
pakuti ukulu wake udzakhala ponseponse pa dziko lapansi.
5 Ndipo Iye adzakhala mtendere wawo.

*Chipulumutso ndi Chiwonongeko*

Asiriya akadzalowa m’dziko lathu
ndi kuyamba kuthira nkhondo malo athu otetezedwa,
tidzawadzutsira abusa asanu ndi awiri,
ngakhalenso atsogoleri asanu ndi atatu.
6 Iwo adzagonjetsa dziko la Asiriya ndi lupanga,
dziko la Nimurodi adzalilamulira mwankhondo.
Adzatipulumutsa kwa Asiriya
akadzafika m’malire a m’dziko lathu
kudzatithira nkhondo.

7 Otsalira a Yakobo adzakhala
pakati pa mitundu yambiri ya anthu
ngati mame ochokera kwa Yehova,
ngati mvumbi pa udzu,
omwe sulamulidwa ndi munthu

kapena kudikira lamulo la anthu.
8 Otsala a Yakobo adzakhala pakati pa mitundu ya anthu,
m'gulu la anthu a mitundu yambiri,
ngati mkango pakati pa nyama za m'nkhalango.
Ngati mwana wa mkango pakati pa gulu la nkhosa,
amene pozidutsa amazidya ndi kuzikhadzula,
ndipo palibe angathe kuzilanditsa.
9 Mudzagonjetsa adani anu,
ndipo adani anu onse adzawonongeka.
10 Yehova akuti,
"Tsiku limenelo ndidzawononga akavalo anu onse
ndi kuphwasula magaleta anu.
11 Ndidzawononga mizinda ya m'dziko mwanu
ndi kugwetsa malinga anu onse.
12 Ndidzawononga ufiti wanu
ndipo sikudzakhalanso anthu owombeza mawula.
13 Ndidzawononga mafano anu osema
pamodzi ndi miyala yanu yopatulika imene ili pakati panu;
simudzagwadiranso zinthu zopanga
ndi manja anu.
14 Ndidzazula mitengo ya mafano a Asera imene ili pakati panu,
ndipo ndidzawononga mizinda yanu.
15 Ndidzayilanga mwaukali ndi mokwiya
mitundu imene sinandimvere Ine."

# 6

*Mlandu wa Yehova ndi Israeli*

1 Tamverani zimene Yehova akunena:
"Nyamukani, fotokozani mlandu wanu pamaso pa mapiri;
zitunda zimve zimene inu muti muyankhule.
2 Imvani mlandu wa Yehova, inu mapiri;
tamverani, maziko amuyaya a dziko lapansi.
Pakuti Yehova ali ndi mlandu ndi anthu ake;
Iye akutsutsa Aisraeli.

3 "Anthu anga, kodi ndakuchitirani chiyani?
Kodi ndakutopetsani bwanji? Ndiyankheni.
4 Ine ndinakutulutsani ku dziko la Igupto
ndi kukuwombolani ku nyumba ya ukapolo.
Ndinatuma Mose kuti akutsogolereni,
pamodzi ndi Aaroni ndi Miriamu.
5 Anthu anga, kumbukirani
zimene Balaki mfumu ya ku Mowabu inafuna kukuchitirani
ndiponso zimene Balaamu mwana wa Beori anayankha.
Kumbukirani zomwe zinachitika pa ulendo wochoka ku Sitimu kupita ku Giligala,
kuti mudziwe machitidwe olungama a Yehova."

6 Kodi ndidzatenga chiyani kupita nacho pamaso pa Yehova
ndi kukagwada pamaso pa Mulungu wakumwamba?
Kodi ndidzabwera pamaso pake ndi nsembe yopsereza,
ndi ana ang'ombe a chaka chimodzi?

7 Kodi Yehova adzakondwera ndi nkhosa zazimuna 1,000,
kapena ndi mitsinje yosalekeza ya mafuta?
Kodi ndipereke nsembe mwana wanga woyamba kubadwa chifukwa cha zolakwa zanga?
Chipatso cha thupi langa chifukwa cha tchimo la moyo wanga?
8 Munthu iwe, Yehova wakuonetsa kale chimene chili chabwino.
Tsono kodi Yehova akuyembekezera chiyani kwa iwe?
Uzichita zolungama ndi kukonda chifundo
ndiponso kuyenda modzichepetsa pamaso pa Mulungu wako.

*Kulakwa kwa Israeli ndi Chilango chake*

9 Tamverani! Yehova akuyitana anthu okhala mu mzinda
ndi nzeru kuopa dzina lanu.
"Mverani mfumu ndi Iye amene anayikhazikitsa.
10 Inu anthu oyipa, kodi Ine n'kuyiwala
chuma chanu chimene munachipeza mwachinyengo,
ndiponso muyeso wanu woperewera umene ndi wotembereredwa?
11 Kodi ndimutenge ngati wosalakwa munthu amene ali ndi sikelo yachinyengo,
ndiponso miyeso yabodza m'thumba lake?
12 Anthu ake olemera amachita zachiwawa;
anthu ake ndi abodza
ndipo pakamwa pawo pamayankhula zachinyengo.
13 Choncho, ndayamba kukuwonongani,
kukusakazani chifukwa cha machimo anu.
14 Mudzadya, koma simudzakhuta;
mudzakhalabe ndi njala.
Mudzasunga zinthu, koma sizidzasungika,
chifukwa zimene mudzasunga zidzawonongedwa ndi lupanga.
15 Mudzadzala, koma simudzakolola.
Mudzayenga mafuta a olivi, koma simudzawagwiritsa ntchito.
Mudzaponda mphesa, koma simudzamwa vinyo wake.
16 Inu mwatsatira malangizo a Omuri
ndiponso machitidwe onse a banja la Ahabu,
ndi khalidwe lawo lonse.
Choncho Ine ndidzakuperekani kuti muwonongedwe
ndiponso anthu anu kuti azunguzike mitu;
mudzanyozedwa ndi anthu a mitundu ina."

# 7

*Chipsinjo cha Israeli*

1 Tsoka ine!
Ndili ngati munthu wokunkha zipatso nthawi yachilimwe,
pa nthawi yokolola mphesa;
palibe phava lamphesa loti n'kudya,
palibe nkhuyu zoyambirira zimene ndimazilakalaka kwambiri.
2 Anthu opembedza atha m'dziko;
palibe wolungama ndi mmodzi yemwe amene watsala.
Anthu onse akubisalirana kuti aphane;
aliyense akusaka m'bale wake ndi khoka.
3 Manja awo onse ndi aluso pochita zoyipa;
wolamulira amafuna mphatso,

woweruza amalandira ziphuphu,
anthu amphamvu amalamula kuti zichitike zimene akuzifuna,
onse amagwirizana zochita.
4 Munthu wabwino kwambiri pakati pawo ali ngati mtengo waminga,
munthu wolungama kwambiri pakati pawo ndi woyipa kuposa mpanda waminga.
Tsiku limene alonda ako ananena lafika,
tsiku limene Mulungu akukuchezera.
Tsopano ndi nthawi ya chisokonezo chawo.
5 Usadalire mnansi;
usakhulupirire bwenzi.
Usamale zoyankhula zako
ngakhale kwa mkazi amene wamukumbatira.
6 Pakuti mwana wamwamuna akunyoza abambo ake,
mwana wamkazi akuwukira amayi ake,
mtengwa akukangana ndi apongozi ake,
adani a munthu ndi amene amakhala nawo m'banja mwake momwe.

7 Koma ine ndikudikira Yehova mwachiyembekezo,
ndikudikira Mulungu Mpulumutsi wanga;
Mulungu wanga adzamvetsera.

*Kuuka kwa Israeli*

8 Iwe mdani wanga, usandiseke!
Ngakhale ndagwa, ndidzauka.
Ngakhale ndikukhala mu mdima,
Yehova ndiye kuwunika kwanga.
9 Ndidzapirira mkwiyo wa Yehova,
chifukwa ndinamuchimwira,
mpaka ataweruza mlandu wanga
ndi kukhazikitsa chilungamo changa.
Iye adzanditulutsa ndi kundilowetsa m'kuwunika;
ndidzaona chilungamo chake.
10 Ndipo mdani wanga adzaona zimenezi
nadzagwidwa ndi manyazi,
iye amene anandifunsa kuti,
"Ali kuti Yehova Mulungu wako?"
Ndidzaona kugonjetsedwa kwake ndi maso anga;
ngakhale tsopano adzaponderezedwa
ngati matope m'misewu.

11 Idzafika nthawi yomanganso makoma anu,
nthawi yokulitsanso malire anu.
12 Nthawi imeneyo anthu adzabwera kwa inu
kuchokera ku Asiriya ndi mizinda ya ku Igupto,
ngakhale kuchokera ku Igupto mpaka ku Yufurate
ndiponso kuchokera ku nyanja ina mpaka ku nyanja inanso
kuchokera ku phiri lina mpaka ku phiri linanso.
13 Dziko lapansi lidzasanduka chipululu
chifukwa cha anthu okhala m'dzikomo, potsatira zochita za anthuwo.

*Pemphero ndi Matamando*

14 Wetani anthu anu ndi ndodo yanu yowateteza,

nkhosa zimene ndi cholowa chanu,
zimene zili zokha m'nkhalango,
m'dziko la chonde.
Muzilole kuti zidye mu Basani ndi mu Giliyadi
monga masiku akale.

15 "Ndidzawaonetsa zodabwitsa zanga,
ngati masiku amene ndinawatulutsa m'dziko la Igupto."

16 Mitundu ya anthu idzaona zimenezi ndipo idzachita manyazi,
ngakhale ali ndi mphamvu zotani.
Adzagwira pakamwa pawo
ndipo makutu awo adzagontha.
17 Adzabwira fumbi ngati njoka,
ngati zolengedwa zomwe zimakwawa pansi.
Adzabwera akunjenjemera kuchokera m'maenje awo;
mwamantha adzatembenukira kwa Yehova Mulungu wathu
ndipo adzachita nanu mantha.
18 Kodi alipo Mulungu wofanana nanu,
amene amakhululukira tchimo ndi kuyiwala zolakwa
za anthu otsala amene ndi cholowa chake?
Inu simusunga mkwiyo mpaka muyaya
koma kwanu n'kuonetsa chikondi chosasinthika.
19 Inu mudzatichitiranso chifundo;
mudzapondereza pansi machimo athu
ndi kuponyera zolakwa zathu zonse pansi pa nyanja.
20 Mudzakhala wokhulupirika kwa Yakobo,
ndi kuonetsa chifundo chanu kwa Abrahamu,
monga munalonjeza molumbira kwa makolo athu
masiku amakedzana.

# Nahumu

1 Uthenga wonena za Ninive. Buku la masomphenya a Nahumu wa ku Elikosi.

### *Mkwiyo wa Yehova pa Ninive*

2 Yehova ndi Mulungu wansanje
ndiponso wobwezera;
Yehova amabwezera ndipo ndi waukali.
Yehova amabwezera adani ake
ndipo ukali wake umakhala nthawi zonse pa adani akewo.
3 Yehova sakwiya msanga koma ndi wa mphamvu yayikulu;
ndipo sadzalola kuti munthu
wolakwa asalangidwe.
Iye amayenda m'kamvuluvulu ndi m'namondwe,
ndipo mitambo ndi fumbi la ku mapazi ake.
4 Amalamulira nyanja ndipo imawuma;
amawumitsa mitsinje yonse.
Zomera za ku Basani ndi Karimeli zimawuma
ndipo maluwa a ku Lebanoni amafota.
5 Mapiri amagwedera pamaso pake
ndipo zitunda zimasungunuka.
Dziko lapansi limanjenjemera pamaso pake,
dziko lonse ndi zonse zokhala m'menemo.
6 Ndani angathe kuyima pamaso pake Iye akalusa?
Ndani angapirire mkwiyo wake woopsa?
Ukali wake ukuyaka ngati moto;
matanthwe akunyeka pamaso pake.

7 Yehova ndi wabwino,
ndiye kothawirako nthawi ya masautso.
Amasamalira amene amamudalira,
8 koma ndi madzi achigumula choopsa
Iye adzawononga adani ake (Ninive);
adzapirikitsira adani ake ku malo a mdima.

9 Chiwembu chilichonse chimene akukonzekera kumuchitira Yehova
adzachiwononga kotheratu;
msautso sudzabweranso kachiwiri.
10 Iwo adzakodwa mu ziyangoyango za minga
ndipo adzaledzera ndi vinyo wawo;
adzatenthedwa ngati ziputu zowuma.
11 Kwa iwe, Ninive, kunachokera munthu wa cholinga choyipa,
wofuna kuchitira Yehova chiwembu,
amene amapereka uphungu woyipa.
12 Yehova akuti,
"Ngakhale Asiriyawo ali ndi abwenzi,
kaya iwowo ndi ambiri,
koma adzawonongedwa ndi kutheratu.
Ngakhale ndinakuzunza iwe Yuda,
sindidzakuzunzanso.
13 Tsopano ndidzathyola goli lake pa khosi lako

ndipo ndidzadula maunyolo ako.”

14 Yehova walamulira za iwe, Ninive kuti,
“Sudzakhala ndi zidzukulu
zimene zidzadziwike ndi dzina lako.
Ndidzawononga zifanizo zosema ndi mafano owumba
amene ali m’nyumba ya milungu yako.
Ine ndidzakukumbira manda
chifukwa ndiwe woyipitsitsa.”
15 Taonani, pa phiripo,
mapazi a munthu amene akubweretsa nkhani yabwino,
amene akulengeza za mtendere!
Inu anthu a ku Yuda, chitani madyerero anu
ndipo kwaniritsani malumbiro anu.
Anthu oyipa sadzakuthiraninso nkhondo;
iwo adzawonongedwa kotheratu.

# 2

*Kugwa kwa Ninive*

1 Wodzathira nkhondo akubwera
kudzalimbana nawe, Ninive.
Tetezani malinga anu,
dziyang’anani ku msewu,
konzekerani nkhondo,
valani dzilimbe.
2 Yehova adzabwezeretsa ulemerero wa Yakobo
ngati ulemerero wa Israeli,
ngakhale anthu owononga anawawononga kotheratu
ndipo anawononganso mpesa wawo.

3 Zishango za ankhondo ake ndi zofiira;
asilikali ake avala zovala zofiirira.
Zitsulo za pa magaleta zikunyezimira
tsiku la kukonzekera kwake.
Akuonetsa mikondo ya mkungudza yonoledwa.
4 Magaleta akuthamanga m’misewu
akungothamangathamanga pa mabwalo.
Akuoneka ngati miyuni yoyaka;
akuthamanga ngati ching’aning’ani.

5 Iye akuyitanitsa asilikali ake wolemekezeka,
koma iwo akubwera napunthwa.
Akuthamangira ku linga la mzinda;
akuyimika chodzitchinjirizira pamalo pake.
6 Atsekula zipata zotchinga madzi a mu mtsinje
ndipo nyumba yaufumu yagwa.
7 Zatsimikizika kuti mzinda
utengedwa ndi kupita ku ukapolo.
Akapolo aakazi akulira ngati nkhunda
ndipo akudziguguda pachifuwa.
8 Ninive ali ngati dziwe,
ndipo madzi ake akutayika.

Iwo akufuwula kuti, “Imani! Imani!”
Koma palibe amene akubwerera.
9 Funkhani siliva!
Funkhani golide!
Katundu wake ndi wochuluka kwambiri,
chuma chochokera pa zinthu zake zamtengowapatali!
10 Iye wawonongedwa, wafunkhidwa ndipo wavulidwa!
Mitima yasweka, mawondo akuwombana,
anthu akunjenjemera ndipo
nkhope zasandulika ndi mantha.

11 Kodi tsopano dzenje la mikango lili kuti,
malo amene mikango inkadyetserako ana ake,
kumene mkango waumuna ndi waukazi unkapitako,
ndipo ana a mkango sankaopa kanthu kalikonse?
12 Mkango waumuna unkapha nyama yokwanira ana ake
ndiponso kuphera nyama mkango waukazi,
kudzaza phanga lake ndi zimene wapha
ndiponso dzenje lake ndi nyama imene waphayo.

13 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
“Ine ndikutsutsana nawe.
Ndidzatentha magaleta ako mpaka utsi tolotolo,
ndipo lupanga lidzapha mikango yako yaying’ono;
sindidzakusiyira chilichonse choti udye pa dziko lapansi.
Mawu a amithenga anu sadzamvekanso.”

# 3

*Tsoka la Ninive*

1 Tsoka kwa mzinda wopha anthu,
mzinda wodzaza ndi mabodza,
mzinda wodzaza ndi anthu olanda zinthu anzawo,
mu mzinda m’mene simusowa anthu osautsidwa nthawi zonse!
2 Kulira kwa zikwapu,
mkokomo wa mikombero,
kufuwula kwa akavalo
ndiponso phokoso la magaleta!
3 Kuthamanga kwa anthu okwera pa akavalo,
kung’anima kwa malupanga
ndi kunyezimira kwa mikondo!
Anthu ambiri ophedwa,
milumilu ya anthu akufa,
mitembo yosawerengeka,
anthu akupunthwa pa mitemboyo.
4 Zonsezi ndi chifukwa cha zilakolako za mkazi wachiwerewere,
wokopa anthu uja, mkazi wochita zamatsenga,
amene anakopa mitundu ya anthu ndi zachiwerewere zake,
ndiponso anthu a mitundu ina ndi zaufiti zake.

5 Yehova Wamphamvuzonse akuti,
“Ine ndikutsutsana nawe.
Ndidzakuvula chovala chako.

Anthu a mitundu ina ndidzawaonetsa umaliseche wako
ndipo udzachita manyazi pamaso pa maufumu onse.
6 Ndidzakuthira zonyansa,
ndidzakuchititsa manyazi
ndiponso kukusandutsa chinthu choseketsa.
7 Onse amene adzakuona adzakuthawa ndipo adzati,
'Ninive wasanduka bwinja,
adzamulira ndani?'
Kodi ndingamupeze kuti munthu woti n'kukutonthoza?"

8 Kodi ndiwe wopambana Tebesi,
mzinda wokhala m'mbali mwa Nailo,
wozunguliridwa ndi madzi?
Mtsinjewo unali chitetezo chake,
madziwo anali linga lake.
9 Mphamvu zake zinali Kusi ndi Igupto,
Puti ndi Libiya anali ena mwa abwenzi ake.
10 Komabe anthu a ku Tebesi anagwidwa
ndipo anapita ku ukapolo.
Ana ake anawaphwanyitsa pansi
m'misewu yonse ya mu mzindamo.
Anachita maere ogawana anthu ake otchuka,
ndipo anthu ake onse amphamvu
anamangidwa ndi maunyolo.
11 Iwenso Ninive udzaledzera;
udzabisala
ndipo udzafunafuna malo othawirako kuopa mdani.

12 Malo ako onse otetezedwa ali ngati mitengo ya mkuyu
yokhala ndi zipatso zoyambirira kucha;
pamene agwedeza mitengoyo,
nkhuyuzo zimagwera m'kamwa mwa wofuna kuzidya.
13 Tayang'ana ankhondo ako,
onse ali ngati akazi!
Zipata za dziko lako zatsekukira adani ako;
moto wapsereza mipiringidzo yake.

14 Tungani madzi woti mudzamwe nthawi ya kuzunguliridwa kwanu,
limbitsani chitetezo chanu!
Pondani dothi,
ikani m'chikombole,
konzani khoma la njerwa!
15 Kumeneko moto udzakupserezani;
lupanga lidzakukanthani
ndipo lidzakuwonongani ngati likuwononga ziwala.
Chulukanani ngati ziwala,
chulukanani ngati dzombe!
16 Mwachulukitsa chiwerengero cha anthu a malonda anu
mpaka kupambana nyenyezi za mlengalenga,
koma iwo ngati dzombe akuwononga dziko
ndipo kenaka akuwuluka n'kuchoka.
17 Akalonga ako ali ngati dzombe,
akuluakulu ako ali ngati gulu la dzombe

limene lamatirira pa khoma nthawi yozizira,
koma pamene dzuwa latuluka limawuluka,
ndipo palibe amene amadziwa komwe lapita.

18 Iwe mfumu ya ku Asiriya,
abusa ako agona tulo;
anthu ako olemekezeka amwalira.
Anthu ako amwazikira ku mapiri
popanda ndi mmodzi yemwe wowasonkhanitsa.
19 Palibe chimene chingachize bala lako;
chilonda chako sichingapole.
Aliyense amene amamva za iwe
amawomba m'manja chifukwa cha kugwa kwako,
kodi alipo amene sanazilawepo
nkhanza zako zosatha?

# Habakuku

1 Uthenga umene mneneri Habakuku analandira m’masomphenya.

### *Dandawulo la Habakuku*

2 Kodi inu Yehova, ndidzakhala ndikukupemphani thandizo kwa nthawi yayitali motani,
koma wosayankha?
Kapena kufuwulira kwa inu kuti, “Chiwawa kuno!”
koma wosatipulumutsa?
3 Chifukwa chiyani mukundionetsa zinthu zoyipa?
Chifukwa chiyani mukundionetsa mavutowa?
Ndikuona chiwonongeko ndi chiwawa;
pali ndewu ndi kukangana kwambiri.
4 Kotero malamulo anu atha mphamvu,
ndipo chilungamo sichikugwira ntchito.
Anthu oyipa aposa olungama,
kotero apotoza chilungamo.

### *Yankho la Yehova*

5 “Yang’anani pakati pa mitundu ya anthu, ndipo penyetsetsani,
ndipo muthedwe nazo nzeru.
Pakuti ndidzachitadi zinthu pa nthawi yanu
zimene inu simudzazikhulupirira,
ngakhale wina atakufotokozerani.
6 Pakuti taonani, Ine ndikuwutsa Ababuloni,
anthu ankhanza ndiponso amphamvu,
amene amapita pa dziko lonse lapansi
kukalanda malo amene si awo.
7 Iwowa ndi anthu ochititsa mantha, ndipo ndi owopsa;
amadzipangira okha malamulo
ndi kudzipezera okha ulemu.
8 Akavalo awo ndi aliwiro kwambiri kupambana akambuku
ndi owopsa kupambana mimbulu yolusa nthawi ya madzulo.
Okwerapo awo akuthamanga molunjika;
a pa akavalo awo ndi ochokera kutali,
akuwuluka ngati chiwombankhanga chofuna kugwira nyama;
9 onse akubwera atakonzekera zachiwawa.
Gulu la ankhondo likubwera ngati mphepo ya m’chipululu
ndi kugwira akapolo ochuluka ngati mchenga.
10 Akunyoza mafumu
ndiponso kuchitira chipongwe olamulira.
Akupeputsa mizinda yonse yotetezedwa;
akumanga mitumbira ndi kulanda mizindayo.
11 Kenaka amasesa mofulumira ngati mphepo n’kumangopitirirabe,
anthu ochimwa, amene mphamvu zawo ndiye mulungu wawo.”

### *Dandawulo Lachiwiri la Habakuku*

12 Inu Yehova, kodi sindinu wachikhalire?
Mulungu wanga, Woyera wanga, ife sitidzafa.
Inu Yehova, munawasankha anthuwo kuti abweretse chiweruzo;
Inu Thanthwe, munawayika iwowo kuti atilange.

13 Maso anu ndi oyera kwambiri safuna kuona choyipa;
Inu simulekerera cholakwa.
Chifukwa chiyani nanga mukulekerera anthu ochita zachinyengowa?
Chifukwa chiyani muli chete pamene anthu oyipa
akuwononga anthu olungama kupambana iwowo?
14 Mwasandutsa anthu kukhala ngati nsomba zam'nyanja,
ngati zolengedwa zam'nyanja zimene zilibe wolamulira.
15 Mdani wawo woyipa amakoka anthu onse ndi mbedza,
amawakola mu ukonde wake,
amawasonkhanitsa mu khoka lake;
kotero iyeyo amakondwa ndi kusangalala.
16 Choncho iye amaperekera nsembe ukonde wake
ndiponso kufukizira lubani khoka lake,
popeza ukonde wakewo ndiye umamubweretsera moyo wapamwamba
ndipo amadya chakudya chabwino kwambiri.
17 Kodi iye azipitirabe kugwiritsa ntchito makoka akewo,
kuwononga mitundu ya anthu mopanda chifundo?

# 2

1 Ndidzakhala pa malo anga aulonda,
ndi kuyima pa mitumbira ya nkhondo;
ndidzadikira kuti ndimve zimene Iye adzandiwuze,
ndi yankho limene ndidzapatsidwe pa madandawulo anga.

*Yankho la Yehova*

2 Tsono Yehova anandiyankha, nati:
"Lemba masomphenyawa
ndipo uwalembe mooneka bwino pa mapale
kuti wowerenga awawerenge mosavuta.
3 Pakuti masomphenyawa akudikira nthawi yake;
masomphenyawa akunena zam'tsogolo
ndipo sizidzalephera kuchitika.
Ngakhale achedwe kukwaniritsidwa, uwayembekezere;
zidzachitika ndithu ndipo sadzachedwa.

4 "Taona, mdani wadzitukumula;
zokhumba zake sizowongoka,
koma wolungama adzakhala ndi moyo mwachikhulupiriro.
5 Ndithu, wasokonezeka ndi vinyo;
ndi wodzitama ndiponso wosakhazikika.
Pakuti ngodzikonda ngati manda,
ngosakhutitsidwa ngati imfa,
wadzisonkhanitsira mitundu yonse ya anthu
ndipo wagwira ukapolo anthu a mitundu yonse.
6 "Kodi onse ogwidwawo sadzamunyoza ndi kumunyogodola ponena
kuti,
"Tsoka kwa amene amadzikundikira katundu amene si wake
ndipo amadzilemeretsa ndi chuma cholanda!
Kodi izi zidzachitika mpaka liti?
7 Kodi angongole ako sadzakuwukira mwadzidzidzi?
Kodi sadzadzuka ndi kukuchititsa mantha?
Pamenepo iwe udzalandidwa kalikonse.
8 Pakuti unafunkha mitundu yambiri ya anthu,

mitundu ina imene inatsala idzakufunkha iweyo.
Pakuti wakhetsa magazi a anthu;
wawononga mayiko ndi mizinda ndi aliyense wokhala m'menemo.

9 "Tsoka kwa amene amalemera ndi chuma chochipeza mwachinyengo,
kukweza malo ake okhalapo,
kuthawa mavuto!
10 Wakonzekera kuwononga mitundu yambiri ya anthu,
kuchititsa manyazi nyumba yako yomwe ndi kuwononga moyo wako.
11 Mwala pa khoma udzafuwula,
ndipo mitanda ya matabwa idzavomereza zimenezi.

12 "Tsoka kwa amene amanga mzinda pokhetsa magazi
ndi kukhazikitsa mzinda pochita zoyipa!
13 Kodi Yehova Wamphamvuzonse sanatsimikize
kuti ntchito za anthu zili ngati nkhuni pa moto,
ndi kuti mitundu ya anthu imadzitopetsa popanda phindu?
14 Pakuti dziko lapansi lidzadzaza ndi chidziwitso cha ulemerero wa Yehova,
monga momwe madzi amadzazira nyanja.

15 "Tsoka kwa amene amamwetsa anzake zakumwa zoledzeretsa,
kutsanula m'botolo mpaka ataledzera,
kuti aone umaliseche wawo.
16 Udzachita manyazi m'malo mokhala ndi ulemerero.
Tsopano ino ndi nthawi yako! Imwa mpaka umaliseche wako uwonekere!
Chikho chochokera m'dzanja lamanja la Yehova chikubwera kwa iwe,
ndipo manyazi adzaphimba ulemerero wako.
17 Udzathedwa nzeru ndi chiwawa chimene unachita ku Lebanoni,
ndiponso udzachita mantha ndi nyama zimene unaziwononga.
Pakuti wakhetsa magazi a anthu;
wawononga mayiko ndi mizinda ndi aliyense wokhala m'menemo.

18 "Kodi fano lili ndi phindu lanji, poti analisema ndi munthu,
kapena chifanizo chimene chimaphunzitsa mabodza?
Pakuti munthu amene walipanga amakhulupirira ntchito ya manja ake;
amapanga mafano amene samatha kuyankhula.
19 Tsoka kwa amene amawuza mtengo kuti, 'Khala wamoyo!'
Kapena mwala wopanda moyo kuti, 'Dzuka!'
Kodi zimenezi zingathe kulangiza?
Ndi zokutidwa ndi golide ndi siliva;
m'kati mwake mulibe mpweya.
20 Koma Yehova ali m'Nyumba yake yopatulika;
dziko lonse lapansi likhale chete pamaso pake."

# 3

### *Pemphero la Habakuku*

1 Pemphero la mneneri Habakuku potsata mayimbidwe a Sigionoti.
2 Inu Yehova, ndamva za kutchuka kwanu;
Inu Yehova, ntchito zanu zandiopsa.
Muzichitenso masiku athu ano,

masiku athu ano zidziwike;
mu ukali wanu mukumbukire kuchita chifundo.

3 Mulungu anabwera kuchokera ku Temani,
Woyerayo kuchokera ku Phiri la Parani.
Sela
Ulemerero wake unaphimba mlengalenga
ndipo dziko lapansi linadzaza ndi matamando ake.
4 Kuwala kwa ulemerero wake kunali ngati kutuluka kwa dzuwa;
kunyezimira kunkatuluka m'dzanja lake,
m'mene anabisamo mphamvu zake.
5 Patsogolo pake pankagwa mliri;
nthenda yoopsa inkagwa kumbuyo kwake.
6 Iye anayimirira ndi kugwedeza dziko lapansi;
anayang'ana ndipo mitundu ya anthu inanjenjemera.
Mapiri okhazikika anagumuka
ndipo zitunda zakalekale zinatitimira.
Njira zake ndi zachikhalire.
7 Ndinaona matenti a ku Kusani ali pa mavuto,
mokhala a ku Midiyani muli ululu waukulu.

8 Inu Yehova, kodi munakwiyira mitsinje?
Kodi munakalipira timitsinje?
Kodi munapsera mtima nyanja
pamene munakwera pa akavalo anu
ndiponso magaleta anu achipulumutso?
9 Munasolola uta wanu m'chimake,
munayitanitsa mivi yambiri.
Sela
Munagawa dziko lapansi ndi mitsinje;
10 mapiri anakuonani ndipo anagwedezeka.
Madzi amphamvu anasefukira;
nyanja yozama inakokoma
ndipo mafunde ake anakwera kwambiri.

11 Dzuwa ndi mwezi zinayima chilili mlengalenga,
pa kung'anima kwa mivi yanu yowulukayo,
pa kunyezimira kwa mkondo wanu.
12 Munayendayenda m'dziko lapansi muli ndi ukali,
ndipo munapondereza mitundu ya anthu muli ndi mkwiyo.
13 Munapita kukalanditsa anthu anu,
kukapulumutsa wodzozedwa wanu.
Munakantha mtsogoleri wa dziko la anthu oyipa,
munawononga anthu ake onse.
Sela
14 Ndi mkondo wake womwe munalasa mtsogoleri wake
pamene ankhondo ake anabwera mwamphamvu kudzatibalalitsa,
ankasangalala ngati kuti akudzawononga
osauka amene akubisala.
15 Munapondaponda pa nyanja ndi akavalo anu,
kuvundula madzi amphamvu.

16 Ndinamva ndipo mtima wanga unagunda kwambiri,

milomo yanga inanjenjemera pakumva phokosolo;
mafupa anga anaguluka,
ndipo mawondo anga anawombana.
Komabe ndikuyembekezera mofatsa,
tsiku la masautso limene lidzafike pa mtundu wa anthu umene ukutithira nkhondo.
17 Ngakhale mtengo wa mkuyu usachite maluwa,
ndipo mipesa ikhale yopanda mphesa.
Ngakhale mitengo ya olivi isabereke zipatso,
ndipo m'minda musatuluke kanthu.
Ngakhale nkhosa
ndi ng'ombe zithe m'khola,
18 komabe ine ndidzakondwera mwa Yehova,
ndidzasangalala mwa Mulungu Mpulumutsi wanga.

19 Ambuye Yehova ndiye mphamvu yanga;
amalimbitsa miyendo yanga ngati ya mbawala yayikazi,
amandithandiza kukafika pamwamba pa phiri.

Kwa mtsogoleri wa mayimbidwe. Pa zoyimbira za nsambo.

# Zefaniya

1 Yehova anayankhula ndi Zefaniya mwana wa Kusi, mwana wa
Gedaliya, mwana wa Amariya, mwana wa Hezekiya pa nthawi ya Yosiya,
mwana wa Amoni, mfumu ya Yuda.

### *Yehova Adzaweruza Dziko Lapansi*

2 “Ndidzawononga kotheratu zinthu zonse
pa dziko lapansi,”
akutero Yehova.
3 “Ndidzawononga anthu pamodzi ndi nyama zomwe;
ndidzawononga mbalame zamlengalenga
ndi nsomba za m’nyanja.
Ndidzawononga anthu oyipa,
ndipo ndidzafafaniza mtundu wa anthu pa dziko lonse lapansi,”
akutero Yehova.

### *Chenjezo kwa Yuda*

4 Ndidzatambasula dzanja langa pa Yuda
ndi onse okhala mu Yerusalemu.
Ndidzawononga pamalo pano otsalira opembedza Baala,
mayina a anthu osapembedza pamodzi ndi ansembe a mafano:
5 amene amagwada pa madenga a nyumba zawo
kupembedza zolengedwa zamumlengalenga,
amene amagwada ndi kulumbira m’dzina la Yehova,
komanso m’dzina la Moleki,
6 amene abwerera m’mbuyo osatsata Yehova,
osafunafuna kapena kupempha nzeru kwa Yehova.
7 Khalani chete pamaso pa Ambuye Yehova,
chifukwa tsiku la Yehova layandikira.
Yehova wakonzekera kupereka nsembe;
wapatula iwo amene wawayitana.
8 Pa tsiku la nsembe ya Yehova
ndidzalanga akalonga
ndi ana aamuna a mfumu
ndi onse amene amavala
zovala zachilendo.
9 Pa tsiku limenelo ndidzalanga
onse amene safuna kuponda pa chiwundo,
amene amadzaza nyumba ya ambuye awo
ndi chiwawa ndi chinyengo.

10 “Pa tsiku limenelo,” akutero Yehova,
“Kufuwula kwakukulu kudzamveka pa Chipata cha Nsomba,
kulira kwa chisoni kuchokera m’Chigawo Chatsopano,
ndi phokoso la kugumuka kochokera ku mapiri.
11 Lirani mwachisoni, inu amene mumakhala kumene kuli msika;
a malonda anu onse adzapululidwa,
ndiponso onse amene ali ndi siliva adzawonongedwa.
12 Pa nthawi imeneyo ndidzafufuzafufuza mu Yerusalemu ndi nyale
ndi kulanga onse amene sakulabadira,

amene ali ngati vinyo wosakhutchumulidwa,
amene amaganiza kuti, ‘Yehova sadzachita chilichonse,
chabwino kaya choyipa.’
13 Chuma chawo chidzafunkhidwa,
nyumba zawo zidzagwetsedwa.
Adzamanga nyumba,
koma osakhalamo;
adzadzala minda ya mpesa
koma sadzamwako vinyo wake.”

### *Tsiku Lalikulu la Yehova*

14 Tsiku lalikulu la Yehova layandikira,
layandikira ndipo lifika msanga.
Tamverani! Kulira kwa pa tsiku la Yehova kudzakhala kowawa,
ngakhale munthu wolimba mtima adzalira kwambiri.
15 Tsiku limenelo lidzakhala la ukali,
tsiku losautsa ndi lomvetsa chisoni,
tsiku la mavuto ndi la chiwonongeko,
tsiku la mdima ndi lachisoni,
tsiku la mitambo ndi la mdima wandiweyani.
16 Tsiku loliza lipenga ndi la mfuwu wankhondo,
tsiku la kugwa kwa mizinda yotetezedwa
ndi nsanja za pa ngodya.
17 Ndidzabweretsa msautso pa anthu
ndipo adzayenda ngati anthu osaona,
chifukwa achimwira Yehova,
magazi awo adzamwazika ngati fumbi
ndi mnofu wawo ngati ndowe.
18 Ngakhale siliva wawo kapena golide wawo
sadzatha kuwapulumutsa
pa tsiku la ukali wa Yehova.
Dziko lonse lapansi lidzanyeka
m’moto wa nsanje yake
chifukwa adzakantha modzidzimutsa
onse okhala pa dziko lapansi.

## 2

1 Sonkhanani pamodzi, sonkhanani pamodzi,
inu mtundu wochititsa manyazi,
2 isanafike nthawi yachiweruzo,
nthawi yanu isanawuluke ngati mungu,
usanakufikeni mkwiyo woopsa wa Yehova,
tsiku la ukali wa Yehova lisanafike pa inu.
3 Funafunani Yehova, inu nonse odzichepetsa a m’dziko,
inu amene mumachita zimene amakulamulani.
Funafunani chilungamo, funafunani kudzichepetsa;
mwina mudzatetezedwa
pa tsiku la mkwiyo wa Yehova.

### *Za Afilisti*

4 Gaza adzasiyidwa
ndipo Asikeloni adzasanduka bwinja.
Nthawi yamasana Asidodi adzakhala wopanda anthu

ndipo Ekroni adzazulidwa.
5 Tsoka inu okhala m'mbali mwa nyanja,
inu mtundu wa Akereti;
mawu a Yehova akutsutsa
iwe Kanaani, dziko la Afilisti.
"Ndidzakuwononga
ndipo palibe amene adzatsale."

6 Dziko la m'mbali mwa nyanja, kumene kumakhala Akereti,
lidzakhala malo a abusa ndi la makola a nkhosa.
7 Malowa adzakhala a anthu otsala a nyumba ya Yuda;
adzapezako msipu.
Nthawi ya madzulo adzagona
m'nyumba za Asikeloni.
Yehova Mulungu wawo adzawasamalira;
adzabwezeretsa mtendere wawo.

*Za Mowabu ndi Amoni*

8 "Ndamva kunyoza kwa Mowabu
ndi chipongwe cha Amoni,
amene ananyoza anthu anga
ndi kuopseza kuti alanda dziko lawo.
9 Choncho, pali Ine Wamoyo,"
akutero Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wa Israeli,
"Ndithu, Mowabu adzasanduka ngati Sodomu,
Amoni adzasanduka ngati Gomora;
malo a zomeramera ndi maenje a mchere,
dziko la bwinja mpaka muyaya.
Anthu anga otsala adzawafunkha;
opulumuka a mtundu wanga adzalandira dziko lawo."

10 Ichi ndi chimene adzalandire chifukwa cha kunyada kwawo,
chifukwa chonyoza ndi kuchitira chipongwe anthu a Yehova Wamphamvuzonse.
11 Yehova adzawachititsa mantha kwambiri
pamene adzawononga milungu yonse ya m'dzikomo.
Ndipo mitundu ya anthu pa dziko lonse idzamulambira,
uliwonse ku dziko la kwawo.

*Za Kusi*

12 "Inunso anthu a ku Kusi,
mudzaphedwa ndi lupanga."

*Za Asiriya*

13 Yehova adzatambasulira dzanja lake kumpoto
ndi kuwononga Asiriya,
kusiya Ninive atawonongekeratu
ndi owuma ngati chipululu.
14 Nkhosa ndi ng'ombe zidzagona pansi kumeneko,
pamodzi ndi nyama zakuthengo za mtundu uliwonse.
Akadzidzi a m'chipululu ndi akanungu
adzakhala pa nsanamira zake.
Kulira kwawo kudzamveka m'mazenera,
m'makomo mwawo mudzakhala zinyalala zokhazokha,
nsanamira za mkungudza zidzakhala poonekera.

15 Umenewu ndiye mzinda wosasamala
umene kale unali wotetezedwa.
Unkanena kuti mu mtima mwake,
“Ine ndine, ndipo palibenso wina wondiposa.”
Taonani lero wasanduka bwinja,
kokhala nyama zakutchire!
Onse owudutsa akuwunyoza
ndi kupukusa mitu yawo.

# 3

*Tsogolo la Yerusalemu*

1 Tsoka kwa mzinda wa anthu opondereza,
owukira ndi odetsedwa!
2 Sumvera aliyense,
sulandira chidzudzulo.
Sumadalira Yehova,
suyandikira pafupi ndi Mulungu wake.
3 Akuluakulu ake ali ngati mikango yobuma,
olamulira ake ndi olusa ngati mimbulu ya nthawi ya madzulo,
zimene pofika mmawa sizisiya chilichonse.
4 Aneneri ake ndi odzikuza;
anthu achinyengo.
Ansembe ake amadetsa malo opatulika
ndipo amaphwanya lamulo.
5 Yehova amene ali pakati pawo ndi wolungama;
Iye salakwa.
Tsiku ndi tsiku amaweruza molungama,
ndipo tsiku lililonse salephera,
komabe ochita zoyipa sachita manyazi n’komwe.
6 “Ndachotseratu mitundu ya anthu;
ndagwetsa malinga awo.
Ndipo sindinasiye ndi mmodzi yemwe m’misewu mwawo,
popanda aliyense wodutsa.
Mizinda yawo yawonongedwa;
palibe aliyense adzatsalemo.
7 Ndinati,
‘Ndithudi, anthu a mu mzindawu adzandiopa
ndi kumvera kudzudzula kwanga!’
Ndipo sindidzawononga nyumba zawo,
kapena kuwalanganso.
Koma iwo anali okonzeka
kuchita mwachinyengo zinthu zonse zimene amachita.
8 Choncho mundidikire,” akutero Yehova,
“chifukwa cha tsiku limene ndidzaperekera umboni.
Ndatsimikiza kusonkhanitsa pamodzi mitundu ya anthu,
kusonkhanitsa maufumu
ndi kutsanulira ukali wanga pa iwo;
mkwiyo wanga wonse woopsa.
Dziko lonse lidzatenthedwa
ndi moto wa mkwiyo wa nsanje yanga.

9 “Pamenepo ndidzayeretsa milomo ya anthu a mitundu yonse
kuti anthu onsewo ayitane dzina la Yehova

ndi kumutumikira Iye pamodzi.
10 Kuchokera kutsidya kwa mitsinje ya ku Kusi
anthu anga ondipembedza, omwazikana,
adzandibweretsera zopereka.
11 Tsiku limenelo simudzachita manyazi
chifukwa cha zoyipa zonse munandichitira,
popeza ndidzachotsa onse mu mzinda uwu
amene amakondwera chifukwa cha kunyada kwawo.
Simudzakhalanso odzikuza
m'phiri langa lopatulika.
12 Koma ndidzasiya pakati panu
anthu ofatsa ndi odzichepetsa,
amene amadalira dzina la Yehova.
13 Aisraeli otsala sadzachitanso zolakwika;
sadzayankhulanso zonama,
ngakhale chinyengo sichidzatuluka m'kamwa mwawo.
Adzadya ndi kugona
ndipo palibe amene adzawachititse mantha."

14 Imba, iwe mwana wamkazi wa Ziyoni;
fuwula mokweza, iwe Israeli!
Sangalala ndi kukondwera ndi mtima wako wonse,
iwe mwana wamkazi wa Yerusalemu!
15 Yehova wachotsa chilango chako,
wabweza mdani wako.
Yehova, Mfumu ya Israeli, ali pakati pako;
sudzaopanso chilichonse.
16 Pa tsiku limenelo adzanena kwa Yerusalemu kuti,
"Usaope, iwe Ziyoni;
usafowoke.
17 Yehova Mulungu wako ali pakati pako,
ali ndi mphamvu yopulumutsa.
Adzakondwera kwambiri mwa iwe,
adzakukhalitsa chete ndi chikondi chake,
adzayimba mokondwera chifukwa cha iwe."

18 "Ndidzakuchotserani zowawa
za pa zikondwerero zoyikika;
n'zolemetsa ndi zochititsa manyazi.
19 Taonani, nthawi imeneyo ndidzathana ndi
onse amene anakuponderezani;
ndidzapulumutsa olumala
ndi kusonkhanitsa amene anamwazika.
Ndidzawayamikira ndi kuwachitira ulemu
m'dziko lililonse mmene anachititsidwa manyazi.
20 Pa nthawi imeneyo ndidzakusonkhanitsani;
pa nthawi imeneyo ndidzakubweretsani ku mudzi kwanu.
Ndidzakuyamikirani ndi kukuchitirani ulemu
pakati pa mitundu ya anthu a dziko lapansi
pamene ndidzabwezeretsa mtendere wanu
inu mukuona,"
akutero Yehova.

# Hagai

*Za Kumanga Nyumba ya Yehova*

1 Chaka chachiwiri cha Mfumu Dariyo, tsiku loyamba la mwezi
wachisanu ndi chimodzi, Yehova anapatsa mneneri Hagai uthenga wopita
kwa Zerubabeli mwana wa Sealatieli, bwanamkubwa wa Yuda, ndiponso
kwa mkulu wa ansembe Yoswa mwana wa Yehozadaki:
2 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Anthu awa amanena kuti, 'Nthawi
sinafike yoti n'kumanga Nyumba ya Yehova.' "
3 Tsono Yehova anayankhula ndi mneneri Hagai kuti, 4 "Kodi ino
ndi nthawi yoti inuyo muzikhala m'nyumba zomanga bwino, pamene
Nyumba yangayi ikanali bwinja?"
5 Tsono zimene Yehova Wamphamvuzonse akunena ndi izi, "Ganizirani
bwino njira zanu. 6 Mwadzala zambiri, koma mwakolola zochepa.
Mumadya, koma simukhuta. Mumamwa, koma ludzu lanu silitha.
Mumavala, koma simumva kutentha. Mumalandira malipiro, koma
ndalama zanu zimatha ngati mwaziyika m'thumba lobowoka."
7 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Ganizirani bwino njira zanu.
8 Pitani ku mapiri ndipo mukatenge matabwa oti mudzamangire Nyumba
yanga, kuti ndikondwere nayo ndi kulandiramo ulemu," akutero Yehova.
9 "Mumayembekezera zambiri, koma taonani mwapeza pang'ono pokha.
Zimene munazibweretsa ku nyumba, Ine ndinazimwaza. N'chifukwa
chiyani?" Akutero Yehova Wamphamvuzonse. "Chifukwa Nyumba yanga
ikanali bwinja, pamene aliyense wa inu watanganidwa kumanga nyumba
yake. 10 Choncho, chifukwa cha inu, mitambo yaleka kugwetsa mvula
ndipo dziko lapansi laleka kutulutsa zomera. 11 Ndabweretsa chilala pa
minda ndi pa mapiri, chilala chawumitsa tirigu, mphesa, mafuta a olivi
ndi chilichonse chimene chimamera pa nthaka, pa anthu ndi pa ng'ombe,
ndi pa ntchito zonse za manja anu."

12 Pamenepo Zerubabeli mwana wa Sealatieli, mkulu wa ansembe Yoswa
mwana wa Yehozadaki, ndi anthu onse otsala anamvera mawu a Yehova
Mulungu wawo ndi uthenga wa Hagai, chifukwa anatumidwa ndi Yehova
Mulungu wawo. Ndipo anthuwo anaopa Yehova.
13 Tsono Hagai, mthenga wa Yehova, anapereka kwa anthuwo uthenga
uwu wa Yehova: "Ine ndili nanu," akutero Yehova. 14 Kotero Yehova
anakhudza mtima wa Zerubabeli mwana wa Sealatieli, bwanamkubwa
wa Yuda, mtima wa Yoswa mwana wa Yehozadaki, mkulu wa ansembe,
ndiponso mitima ya anthu onse otsala. Iwo anabwera ndi kuyamba
ntchito yomanga Nyumba ya Yehova Wamphamvuzonse, Mulungu wawo,
15 pa tsiku la 24 la mwezi wachisanu ndi chimodzi, wa chaka chachiwiri
cha Mfumu Dariyo.

## 2

*Ulemerero wa Nyumba Yatsopano ya Yehova*

1 Pa tsiku la 21 la mwezi wachisanu ndi chiwiri, Yehova anayankhula
kudzera mwa mneneri Hagai kuti: 2 "Yankhula kwa Zerubabeli mwana wa
Sealatieli, bwanamkubwa wa Yuda, kwa Yoswa mwana wa Yehozadaki,

mkulu wa ansembe, ndi kwa anthu onse otsala. Afunse kuti, 3 'Kodi
alipo amene watsala pakati panu amene anaona ulemerero wakale wa
Nyumba iyi? Nanga tsopano ikuoneka motani kwa inu? Kodi sikuoneka
ngati yopanda pake kwa inu? 4 Iwe Zerubabeli, limba mtima tsopano,'
akutero Yehova. 'Limba mtima, iwe Yoswa mwana wa Yehozadaki,
mkulu wa ansembe. Limbani mtima, anthu nonse a m'dziko,' akutero
Yehova, 'ndipo gwirani ntchito. Pakuti ine ndili nanu,' akutero Yehova
Wamphamvuzonse. 5 'Izi ndi zimene ndinapangana nanu pamene
munkatuluka ku Igupto. Ndipo Mzimu wanga uli pakati panu. Musachite
mantha.'
6 "Yehova Wamphamvuzonse akuti, 'Pakapita nthawi pang'ono
ndidzagwedezanso thambo ndi dziko lapansi, nyanja ndi mtunda.
7 Ndidzagwedeza mitundu yonse ya anthu, ndipo chimene mitundu
yonse ya anthu imachifuna chidzabwera, ndipo ndidzaza Nyumba ino
ndi ulemerero,' akutero Yehova Wamphamvuzonse. 8 'Siliva yense ndi
wanga, golide yense ndi wanganso,' akutero Yehova Wamphamvuzonse.
9 'Ulemerero wa nyumba iyi udzaposa ulemerero wa nyumba yoyamba
ija,' akutero Yehova Wamphamvuzonse. 'Ndipo pamalo pano ndidzak-
hazikitsapo mtendere,' akutero Yehova Wamphamvuzonse."

### *Madalitso kwa Anthu Oyipitsidwa*

10 Chaka chachiwiri cha Dariyo, pa tsiku la 24 la mwezi wachisanu
ndi chinayi, Yehova anayankhula ndi mneneri Hagai kuti: 11 "Yehova
Wamphamvuzonse akuti, 'Funsa ansembe za zimene lamulo likunena:
12 Ngati munthu wakulunga nyama yopatulika mu mkanjo wake, ndipo
mkanjowo n'kukhudza buledi kapena msuzi, kapena vinyo, mafuta
kapena chakudya cha mtundu wina uliwonse, kodi zimenezo zimasan-
duka zopatulika?' "
Ansembe anayankha kuti, "Ayi."
13 Pamenepo Hagai anati, "Ngati munthu amene anayipitsidwa
pokhudza mtembo akhudza chimodzi cha zinthu zimenezi, kodi chinthu-
cho chimayipitsidwa?"
Ansembe anayankha kuti, "Inde, chimayipitsidwa."
14 Pamenepo Hagai anati, " 'Ndi mmene zilili ndi anthu awa ndi dziko
ili pamaso panga,' akutero Yehova. 'Chilichonse amachita ndiponso
chilichonse chimene amapereka n'chodetsedwa.
15 " 'Tsopano muganizire zimenezi kuyambira lero mpaka m'tsogolo.
Ganizirani momwe zinthu zinalili asanayambe kumanga nyumba ya
Yehova. 16 Pamene munthu ankayembekezera miyeso ya tirigu makumi
awiri ankangopeza khumi yokha. Munthu akapita kuti akatunge miyeso
makumi asanu ya vinyo mu mtsuko, ankangopeza miyeso makumi awiri
yokha. 17 Ndinawononga ntchito yonse ya manja anu ndi chinsikwi,
chiwawu ndi matalala, komabe inu simunatembenukire kwa Ine,' akutero
Yehova 18 'Kuyambira lero tsiku la 24 la mwezi wachisanu ndi chinayi
mpaka m'tsogolo, chonde ganizirani bwino tsiku limene munayika maziko
a nyumba ya Yehova. Ganizirani bwino. 19 Kodi m'nkhokwe mwatsala
mbewu? Mpaka lero, mpesa ndi mtengo wa mkuyu, makangadza ndi
mtengo wa olivi sizinabereke zipatso.
" 'Kuyambira lero mpaka m'tsogolo ndidzakudalitsani.' "

### *Zerubabeli Mphete Yolamulira ya Yehova*

20 Yehova anayankhula ndi Hagai kachiwiri, pa tsiku la 24 la mwezi kuti:
21 "Uza Zerubabeli, bwanamkubwa wa Yuda, kuti ndidzagwedeza thambo

ndi dziko lapansi. 22 Ndidzagwetsa mipando yaufumu ndi kuwononga
mphamvu za maufumu achilendo. Ndidzagubuduza magaleta ndi okwerapo ake; akavalo ndi okwerapo ake adzagwa, aliyense adzaphedwa ndi lupanga la m'bale wake.
23 " 'Tsiku limenelo,' akutero Yehova Wamphamvuzonse, 'ndidzakutenga, iwe mtumiki wanga Zerubabeli mwana wa Sealatieli,' akutero Yehova, 'ndipo ndidzakusandutsa kukhala mphete yanga yolamulira, pakuti ndasankha iwe,' akutero Yehova Wamphamvuzonse."

# Zekariya

*Yuda Abwerera kwa Yehova*

1 Mwezi wachisanu ndi chitatu, m'chaka chachiwiri cha ulamuliro wa
Dariyo, Yehova anayankhula ndi mneneri Zekariya mwana wa Berekiya,
mwana wa Ido, kuti:
2 "Yehova anakwiya kwambiri ndi makolo anu. 3 Choncho awuze
anthuwa kuti, 'Yehova Wamphamvuzonse akuti, 'Bwererani kwa Ine,'
akutero Yehova Wamphamvuzonse. 'Ndipo Ine ndidzabwerera kwa inu,'
akutero Yehova Wamphamvuzonse. 4 Musakhale ngati makolo anu,
amene aneneri akale anawalalikira kuti: Yehova Wamphamvuzonse akuti,
'Tsopano lekani njira zanu zoyipa ndi machitidwe anu oyipawo.' Koma
iwo sanamvere kapena kulabadira za Ine, akutero Yehova. 5 Kodi makolo
anuwo ali kuti tsopano? Nanga aneneri, kodi amakhalapo mpaka muyaya?
6 Kodi mawu anga ndi malangizo anga, amene ndinawawuza atumiki anga
aneneri, suja anawachitira makolo anu?
"Tsono iwo analapa ndi kunena kuti, 'Yehova Wamphamvuzonse
watichitira zomwe zikuyenera njira zathu ndi machitidwe athu, monga
anatsimikiza kuti adzachita.' "

*Munthu Pakati pa Mitengo ya Mchisu*

7 Tsiku la 24 la mwezi wa 11, mwezi wa Sebati, chaka chachiwiri
cha ulamuliro wa Dariyo, Yehova anayankhula ndi Zekariya mwana wa
Berekiya, mwana wa Ido.
8 Nthawi ya usiku ndinaona masomphenya. Ndinaona munthu atakwera
pa kavalo wofiira. Iye anayima pakati pa mitengo ya mchisu m'chigwa.
Kumbuyo kwake kunali akavalo ofiira, akhofi ndi oyera.
9 Ine ndinafunsa kuti, "Mbuye wanga, kodi zimenezi ndi chiyani?"
Mngelo amene amayankhula nane anayankha kuti, "Ndidzakuonetsa
kuti zimenezi ndi chiyani."
10 Pamenepo munthu amene anayima pakati pa mitengo ya mchisu
anafotokoza kuti, "Amenewa ndiwo amene Yehova wawatuma kuti
ayendere dziko lonse lapansi."
11 Ndipo okwera pa akavalo enawo anafotokoza kwa mngelo wa Yehova,
amene anayima pakati pa mitengo ya mchisu kuti, "Ife tayendera dziko
lonse lapansi ndipo tapeza kuti dziko lonselo lili pa bata ndi mtendere."
12 Tsono mngelo wa Yehova anati, "Yehova Wamphamvuzonse, kodi
mpaka liti mudzakhala osaonetsa chifundo chanu kwa Yerusalemu ndi
mizinda ya Yuda, amene mwawakwiyira kwa zaka izi 70?" 13 Choncho
Yehova anayankhula mawu abwino ndi achitonthozo kwa mngelo amene
ankayankhula nane.
14 Pamenepo mngelo amene ankayankhula nane anati, "Lengeza
mawu awa: Yehova Wamphamvuzonse akuti, 'Ine ndikuchitira nsanje
Yerusalemu ndi Ziyoni, 15 koma ndakwiya kwambiri ndi anthu a mitundu
ina amene akuganiza kuti ali pa mtendere. Ndinakwiyira anthu anga
pang'ono pokha, koma iwo anawonjeza kuzunza anthu angawo.'
16 "Choncho, Yehova akuti, 'Ndidzabwerera ku Yerusalemu ndi mtima
wachifundo, nyumba yanga adzayimanganso kumeneko. Ndipo adza-
tenganso chingwe choyezera kuti amange Yerusalemu,' akutero Yehova
Wamphamvuzonse.

17 “Lengezanso kuti, Yehova Wamphamvuzonse akuti, ‘Mizinda yanga idzakhalanso ndi zokoma zosefukira ndipo Yehova adzatonthoza Ziyoni ndi kusankhanso Yerusalemu.’ ”

### *Nyanga Zinayi ndi Amisiri Azitsulo Anayi*

18 Kenaka ndinayang’ananso, ndipo patsogolo panga panali nyanga
zinayi. 19 Ndinamufunsa mngelo amene amayankhula nane kuti, “Kodi
zimenezi ndi chiyani?”

Iye anandiyankha kuti, “Izi ndi nyanga zimene zinabalalitsa Yuda, Israeli ndi Yerusalemu.”

20 Kenaka Yehova anandionetsa amisiri azitsulo anayi. 21 Ndinafunsa
kuti, “Amisiri a zitsulowa akudzachita chiyani?”

Iye anayankha kuti, “Izi ndi nyanga zimene zinabalalitsa Yuda kotero kuti panalibe wina amene akanalimbana nazo, koma amisiri a zitsulowa abwera kudzaziopseza ndi kugwetsa nyanga zimenezi za mitundu ya anthu amene analimbana ndi dziko la Yuda ndi kubalalitsa anthu ake.”

## 2

### *Munthu ndi Chingwe Choyezera*

1 Kenaka ndinayang’ananso, ndipo ndinaona munthu atanyamula
chingwe choyezera m’manja mwake. 2 Ndipo ndinafunsa kuti, “Kodi
ukupita kuti?”

Anandiyankha kuti, “Akukayeza Yerusalemu kuti ndidziwe mulifupi mwake ndi mulitali mwake.”

3 Taonani, mngelo amene amayankhula nane uja akuchoka, mngelo
wina anabwera kudzakumana naye 4 ndipo anamuwuza kuti, “Thamanga,
kamuwuze mnyamatayo kuti, ‘Yerusalemu udzakhala mzinda wopanda
malinga chifukwa mudzakhala anthu ambiri ndiponso ziweto zochuluka.
5 Ndipo Ine mwini ndidzakhala linga lamoto kuteteza mzindawo,’ akutero
Yehova, ‘ndipo ndidzakhala ulemerero m’kati mwake.’

6 “Tulukani! Tulukani! Thawaniko ku dziko la kumpoto,” akutero Yehova, “pakuti ndinakumwazirani ku mphepo zinayi zamlengalenga,” akutero Yehova.

7 “Tuluka, iwe Ziyoni! Thawa, iwe amene umakhala m’dziko la mwana
wamkazi wa Babuloni!” 8 Pakuti Yehova Wamphamvuzonse akuti, “Atatha
kundilemekeza wanditumiza kwa anthu a mitundu ina amene anaku-
funkhani; pakuti aliyense wokhudza inu wakhudza mwanadiso wanga.
9 Ndithu Ine ndidzawamenya anthuwo ndi dzanja langa ndipo amene
anali akapolo awo ndiye adzawalande zinthu. Pamenepo mudzadziwa
kuti Yehova Wamphamvuzonse ndiye wandituma.

10 “Iwe mwana wamkazi wa Ziyoni, fuwula ndipo sangalala. Pakuti
taona ndikubwera, ndipo ndidzakhala pakati pako,” akutero Yehova.
11 “Nthawi imeneyo anthu a mitundu yambiri adzabwera kwa Yehova
ndipo adzasanduka anthu anga. Ndidzakhala pakati pako ndipo iwe
udzadziwa kuti Yehova Wamphamvuzonse wandituma kwa iwe. 12 Yehova
adzachititsa kuti Yuda akhale chuma chake m’dziko lopatulika ndipo
adzasankhanso Yerusalemu. 13 Khalani chete pamaso pa Yehova anthu
nonse, chifukwa Iye wavumbuluka kuchoka ku malo ake opatulika.”

## 3

### *Zovala Zoyera za Mkulu wa Ansembe*

1 Pamenepo anandionetsa Yoswa, mkulu wa ansembe, atayima pamaso
pa mngelo wa Yehova, ndipo Satana anayima ku dzanja lake lamanja kuti
atsutsane naye. 2 Yehova anawuza Satana kuti, "Yehova akukudzudzula
iwe Satana! Yehova amene wasankha Yerusalemu akukudzudzula! Kodi
munthu uyu sali ngati chikuni choyaka chofumula pa moto?"

3 Tsono Yoswa anali atavala zovala zalitsiro pa nthawi imene anayima
pamaso pa mngelo. 4 Mngelo uja anawuza anzake amene anali naye kuti,
"Muvuleni zovala zake zalitsirizo."

Kenaka anawuza Yoswa kuti, "Taona, ndachotsa tchimo lako, ndipo
ndikuveka zovala zokongola."

5 Ndipo ine ndinati, "Muvekeni nduwira yopatulika pamutu pake."
Choncho anamuveka nduwira yopatulika pamutu pake, namuvekanso
zovala zatsopano. Nthawiyi n'kuti mngelo wa Yehova atayima pambali.

6 Mngelo wa Yehova analimbikitsa Yoswa kuti, 7 "Yehova Wamphamvu-
zonse akuti, 'Ngati uyenda m'njira zanga ndi kusunga malamulo anga,
pamenepo udzalamulira nyumba yanga ndi kuyang'anira mabwalo anga,
ndipo ndidzakulolani kuti mudzakhale pamodzi ndi amene ali panowa.

8 " 'Mvera tsono, iwe Yoswa mkulu wa ansembe, pamodzi ndi anzako
amene wakhala nawowa, amene ndi chizindikiro cha zinthu zimene
zikubwera: Ine ndidzabweretsa mtumiki wanga, wotchedwa Nthambi.
9 Taona, mwala wokongola umene ndayika patsogolo pa Yoswa! Pa mwala
umenewu pali maso asanu ndi awiri, ndipo Ine ndidzalembapo mawu,'
akutero Yehova Wamphamvuzonse, 'ndipo ndidzachotsa tchimo la dziko
lino tsiku limodzi.

10 " 'Tsiku limenelo aliyense adzayitana mnzake kuti akhale pansi pa
mtengo wamphesa ndi wa mkuyu,' akutero Yehova Wamphamvuzonse."

# 4

*Choyikapo Nyale cha Golide ndi Mitengo Iwiri ya Olivi*

1 Kenaka mngelo amene amayankhula nane anabwerera nandidzutsa,
ngati mmene amadzutsira munthu amene ali m'tulo. 2 Anandifunsa kuti,
"Kodi ukuona chiyani?"

Ndinayankha kuti, "Ine ndikuona choyikapo nyale, chonse chagolide ndi
mbale pamwamba pake ndi nyale zoyaka zisanu ndi ziwiri, iliyonse ili
ndi zibowo zisanu ndi ziwiri zolowetsera zingwe zoyatsira. 3 Ndiponso
pambali pake pali mitengo ya olivi iwiri, umodzi uli kumanja kwa mbaleyo
ndipo winawo kumanzere."

4 Ndinamufunsa mngelo amene amayankhula nane kuti, "Kodi zimenezi
n'chiyani mbuye wanga?"

5 Iye anandiyankha kuti, "Kodi iwe sukuzidziwa zimenezi?"

Ndinayankha kuti, "Ayi mbuye wanga."

6 Choncho iye anandiwuza kuti, "Mawu a Yehova kwa Zerubabeli ndi
awa: 'Osati mwa nkhondo kapena ndi mphamvu, koma ndi Mzimu
wanga,' akutero Yehova Wamphamvuzonse.

7 "Kodi ndiwe yani, iwe phiri lamphamvu? Pamaso pa Zerubabeli
udzasanduka dziko losalala. Pamenepo adzabweretsa mwala wotsiriza.
Akamadzawuyika pamwamba anthu adzafuwula kuti, 'Mulungu adalitse
Nyumbayi! Mulungu adalitse Nyumbayi!' "

8 Ndipo Yehova anayankhulanso nane kuti, 9 "Manja a Zerubabeli ndiwo
ayika maziko a Nyumbayi; adzatsiriza ndi manja ake omwewo. Pamenepo
iwe udzadziwa kuti Yehova Wamphamvuzonse ndiye anakutuma.

10 “Ndani wanyoza tsiku la zinthu zazing’ono? Anthu adzasangalala akadzaona chingwe choyezera m’manja mwa Zerubabeli.

(“Nyale zisanu ndi ziwirizi ndi maso a Yehova, amene amayang’anayang’ana pa dziko lapansi.”)

11 Kenaka ndinafunsa mngelo uja kuti, “Kodi mitengo ya olivi iwiri ili kumanja ndi kumanzere kwa choyikapo nyalechi ikutanthauza chiyani?”

12 Ndinamufunsanso kuti, “Kodi nthambi ziwiri za mtengo wa olivi zomwe zili pambali pa mipopi yodzera mafuta iwiri yagolide zikutanthauza chiyani?”

13 Iye anandiyankha kuti, “Kodi iwe sukuzidziwa zimenezi?”

Ine ndinati, “Ayi mbuye wanga.”

14 Choncho iye anati, “Amenewa ndi anthu awiri amene adzozedwa kuti atumikire Ambuye pa dziko lonse lapansi.”

# 5

### *Chikalata Chowuluka*

1 Ndinayang’ananso ndipo taonani ndinaona chikalata chimene chimawuluka.

2 Mngelo uja anandifunsa kuti, “Kodi ukuona chiyani?”

Ndinayankha kuti, “Ndikuona chikalata chikuwuluka, mulitali mwake mamita asanu ndi anayi ndipo mulifupi mwake mamita anayi ndi theka.”

3 Ndipo mngeloyo anandiwuza kuti, “Awa ndi matemberero amene
akupita pa dziko lonse lapansi; potsata zimene zalembedwa m’kati mwa
chikalatamo, aliyense wakuba adzachotsedwa, ndipo potsata zomwe
zalembedwa kunja kwake, aliyense wolumbira zabodza adzachotsed-
wanso. 4 Yehova Wamphamvuzonse akunena kuti, ‘Temberero limeneli
ndidzalitumiza, ndipo lidzalowa m’nyumba ya munthu wakuba ndi
munthu wolumbira zabodza m’dzina langa. Lidzakhala m’nyumbamo
mpaka kuyiwonongeratu, matabwa ake ndi miyala yake yomwe.’ ”

### *Mkazi mu Dengu*

5 Kenaka mngelo amene amayankhula nane uja anabwera patsogolo panga ndipo anandiwuza kuti, “Kweza maso ako tsopano kuti uwone kuti ndi chiyani chikubwerachi.”

6 Ndinafunsa kuti, “Kodi chimenechi n’chiyani?”

Mngeloyo anayankha kuti, “Limeneli ndi dengu loyezera.” Ndipo anawonjezera kunena kuti, “Umenewu ndi uchimo wa anthu m’dziko lonse.”

7 Pamenepo chovundikira chake chamtovu chinatukulidwa, ndipo
m’dengumo munali mutakhala mkazi. 8 Mngeloyo anati, “Chimenechi
ndi choyipa,” ndipo anamukankhira mkaziyo m’dengu muja, nabwezera
chovundikira chamtovu chija pamwamba pake.

9 Kenaka ndinayang’ananso, ndipo ndinaona akazi awiri akuwuluka kubwera kumene kunali ine; akuwuluzika ndi mphepo. Iwo anali ndi mapiko ngati a kakowa, ndipo ananyamula dengu lija, kupita nalo pakati pa mlengalenga ndi dziko lapansi.

10 Ine ndinafunsa mngelo amene amayankhula nane kuti, “Dengulo akupita nalo kuti?”

11 Iye anayankha kuti, “Ku dziko la Babuloni kuti akalimangire nyumba. Nyumbayo ikadzatha, adzayikamo dengulo.”

# 6

*Magaleta Anayi*

1 Ndinayang'ananso ndipo taonani ndinaona magaleta anayi akutuluka
pakati pa mapiri awiri, mapiri amkuwa. 2 Galeta loyamba limakokedwa
ndi akavalo ofiira, lachiwiri ndi akavalo akuda, 3 lachitatu ndi akavalo oy-
era, ndipo lachinayi ndi akavalo otuwa a mawanga ofiirira, onsewa anali
akavalo amphamvu kwambiri. 4 Ndinafunsa mngelo amene amayankhula
nane uja kuti, "Kodi mbuye wanga chimenechi n'chiyani?"
5 Mngeloyo anandiyankha kuti, "Imeneyi ndi mizimu inayi
yakumwamba, imene ikuchokera pamaso pa Ambuye wa dziko lonse.
6 Galeta la akavalo akuda likupita ku dziko la kumpoto, galeta la akavalo
oyera likutsatira, ndipo galeta la akavalo amawanga ofiirira likupita ku
dziko la kummwera."
7 Pamene akavalo amphamvuwa ankapita, anali ndi changu chofuna
kuyendera dziko lapansi. Ndipo iye anati, "Pitani, kayendereni dziko
lapansi!"
8 Pamenepo anandiyitana, "Taona, akavalo amene apita ku dziko la
kumpoto apumulitsa Mzimu wanga kumeneko."

*Chipewa Chaufumu cha Yoswa*

9 Yehova anayankhula nane kuti, 10 "Landira mphatso kuchokera kwa
anthu amene abwera ku ukapolo, Helidai, Tobiya ndi Yedaya, amene
achokera ku Babuloni. Tsiku lomwelo pita ku nyumba ya Yosiya mwana
wa Zefaniya. 11 Tenga siliva ndi golide upange chipewa chaufumu,
ndipo uchiyike pamutu pa mkulu wa ansembe, Yoswa mwana wa
Yehozadaki. 12 Muwuze kuti zimene akunena Yehova Wamphamvuzonse
ndi izi: 'Taonani, munthu wotchedwa Nthambi ndi ameneyu, ndipo
adzaphuka pomwe alipo ndi kumanga Nyumba ya Yehova. 13 Ndiye amene
adzamange Nyumba ya Yehova, adzalandira ulemerero waufumu ndipo
adzalamulira pa mpando wake waufumu. Adzakhalanso wansembe pa
mpando wake waufumu. Ndipo padzakhala mtendere.' 14 Chipewa cha
ufumucho adzachipereka kwa Helemu, Tobiya, Yedaya, ndi kwa Heni
mwana wa Zefaniya, kuti chikhale chikumbutso m'Nyumba ya Yehova.
15 Anthu okhala kutali adzabwera kudzathandiza kumanga Nyumba ya
Yehova, ndipo iwe udzadziwa kuti Yehova Wamphamvuzonse wanditumа
kwa iwe. Zimenezi zidzachitika ngati mudzamvera mwachangu Yehova
Mulungu wanu."

# 7

*Chiweruzo Cholungama ndi Chifundo, Osati Kusala Zakudya*

1 Pa chaka chachinayi cha Mfumu Dariyo, pa tsiku lachinayi la Kisilevi,
mwezi wachisanu ndi chinayi, Yehova anayankhula ndi Zekariya. 2 Anthu
a ku Beteli anali atatuma Sarezeri ndi Regemu-Meleki pamodzi ndi anthu
awo, kuti akapemphe chifundo kwa Yehova 3 pokafunsa kwa ansembe
a ku Nyumba ya Yehova Wamphamvuzonse ndi aneneri kuti, "Kodi
ine ndizilira ndi kusala zakudya pa mwezi wachisanu, monga mmene
ndakhala ndikuchitira pa zaka zambiri?"
4 Pamenepo Yehova Wamphamvuzonse anayankhula nane kuti, 5 "Funsa
anthu onse a m'dziko ndi ansembe kuti, 'Pamene munkasala zakudya
pa mwezi wachisanu ndi wachisanu ndi chiwiri pa zaka 70 zapitazi,
kodi munkasala chifukwa cha Ine? 6 Ndipo pamene munkadya ndi

kumwa, kodi simunkachita zimenezi podzisangalatsa nokha? 7 Kodi awa
si mawu amene Yehova ankanena kudzera mwa aneneri oyamba aja
pamene Yerusalemu ndi mizinda yake yozungulira anali pa mtendere ndi
pa ulemerero, ndi pamene Negevi ndi ku madera akumadzulo a m'mbali
mwa phiri munali anthu?' "

8 Ndipo Yehova anayankhulanso ndi Zekariya kuti, 9 "Yehova
Wamphamvuzonse akuti, 'Muziweruza molungama; muzichitirana chi-
fundo ndi kumverana chisoni. 10 Musamazunze akazi amasiye kapena
ana amasiye, alendo kapena osauka. Musamaganizirane zoyipa m'mitima
mwanu.'

11 "Koma makolo anu anakana kumvera uthenga umenewu;
anawumitsa mtima nandifulatira, natseka makutu awo kuti asamve.
12 Anawumitsa mitima yawo ngati mwala wa sangalabwi ndipo sanamvere
lamulo kapena mawu amene Yehova Wamphamvuzonse anawatumiza
mwa Mzimu wake kudzera mwa aneneri oyamba aja. Kotero Yehova
Wamphamvuzonse anakwiya kwambiri.

13 " 'Pamene ndinawayitana, iwo sanamvere; choncho pamene iwo
anandiyitana, Ine sindinamverenso,' akutero Yehova Wamphamvuzonse.
14 'Ndinawamwaza ndi kamvuluvulu pakati pa mitundu yonse ya anthu,
kumene anali alendo. Dziko lawo linatsala litasakazidwa kwambiri
kotero kuti palibe amene amabwera kapena kupitamo. Umu ndi mmene
anasandutsira dziko labwino kukhala chipululu.' "

# 8

*Yehova Alonjeza Kudalitsa Yerusalemu*

1 Awa ndi mawu amene Yehova Wamphamvuzonse ananena. 2 Yehova
Wamphamvuzonse akuti, "Ine ndikuchitira nsanje yayikulu Ziyoni. Mtima
wanga ukupweteka chifukwa cha nsanje pa iyeyo."

3 Yehova akuti, "Ndidzabwerera ku Ziyoni ndi kukakhala ku Yerusalemu.
Pamenepo Yerusalemu adzatchedwa Mzinda wa Choonadi ndipo phiri la
Yehova Wamphamvuzonse lidzatchedwa Phiri Lopatulika."

4 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Abambo ndi amayi okalamba adza-
khalanso m'misewu ya mu Yerusalemu, aliyense ali ndi ndodo m'manja
mwake chifukwa cha kuchuluka kwa masiku ake. 5 Ndipo misewu ya mu
mzindamo idzadzaza ndi anyamata ndi atsikana akusewera."

6 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Ngati zikuoneka kuti n'zosatheka
kwa anthu otsala pa nthawi ino, kodi zidzakhala zosathekanso kwa Ine?"
akutero Yehova Wamphamvuzonse.

7 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Taonani ndidzapulumutsa
anthu anga kuchokera ku mayiko a kummawa ndi kumadzulo.
8 Ndidzawabweretsa kuti adzakhale mu Yerusalemu; adzakhala anthu
anga, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wawo, wokhulupirika ndi
wolungama pakati pawo."

9 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Inu amene tsopano mukumva
mawu awa amene akuyankhula aneneri amene analipo pamene ankayika
maziko a nyumba ya Yehova Wamphamvuzonse, 'limbani mtima kuti mu-
mange Nyumba ya Yehova.' 10 Mpaka nthawi imeneyi panalibe munthu
wolandira malipiro pa ntchito kapena ndalama zolipirira nyama zogwira
ntchito. Panalibe munthu amene ankadzigwirira ntchito mwamtendere
chifukwa choopa adani ake, pakuti Ine ndinkawayambanitsa. 11 Koma
tsopano sindidzachitira otsala mwa anthu awa zomwe ndinachita kale,"
akutero Yehova Wamphamvuzonse.

12 “Pakuti mbewu zidzamera bwino, mpesa udzabala zipatso zake,
nthaka idzatulutsa zomera zake, ndi thambo lidzagwetsa mame. Ndidza-
pereka zonse kukhala cholowa cha otsala mwa anthu awa. 13 Monga
mwakhala muli chinthu chotembereredwa pakati pa mitundu ina ya
anthu, inu Yuda ndi Israeli, choncho ndidzakupulumutsani, ndipo mudza-
khala dalitso. Musachite mantha, koma limbani mtima.”
14 Yehova Wamphamvuzonse akuti, “Monga ndinatsimikiza mtima kub-
weretsa choyipa pa inu, komanso osakuchitirani chisoni pamene makolo
anu anandikwiyitsa,” akutero Yehova, 15 “Choncho tsopano ndatsimikiza
mtima kuchitiranso zabwino Yerusalemu ndi Yuda. Musachite mantha.
16 Zinthu zoti muchite ndi izi: Muziwuzana zoona zokhazokha, muzi-
weruza moona ndi mwachilungamo m’mabwalo anu; 17 musamachitire
mnzanu chiwembu, musamakonde kulumbira zonama. Zonsezi Ine
ndimadana nazo,” akutero Yehova.
18 Yehova Wamphamvuzonse anayankhulanso nane. 19 Ndipo ananena
kuti, “Kusala zakudya kwa pa mwezi wachinayi, chisanu, chisanu ndi
chiwiri ndi wakhumi, kudzakhala nthawi yachimwemwe, ya chisangalalo
ndi nthawi ya madyerero chikondwerero kwa Yuda. N’chifukwa chake
muzikonda choonadi ndi mtendere.”
20 Yehova Wamphamvuzonse akuti, “Anthu a mitundu yambiri ndi
anthu okhala m’mizinda yambiri adzabwerabe, 21 ndipo nzika za
mzinda wina zidzapita ku mzinda wina, kukanena kuti, ‘Tiyeni
mwamsanga tikapemphe madalitso kwa Yehova ndi kukapembedza
Yehova Wamphamvuzonse. Inenso ndikupita kumeneko.’ 22 Anthu
ambiri ndiponso a ku mayiko amphamvu adzabwera ku Yerusalemu
kudzapembedza Yehova Wamphamvuzonse ndi kudzapempha madalitso.”
23 Yehova Wamphamvuzonse akuti, “Masiku amenewo anthu khumi
ochokera ku mitundu ya anthu a ziyankhulo zosiyana adzagwira mkanjo
wa Myuda ndi kunena kuti, ‘Tipite nawo, chifukwa tamva kuti Mulungu
ali nanu.’ ”

# 9

*Chiweruzo pa Adani a Israeli*

*Ulosi*

1 Mawu a Yehova odzudzula dziko la Hadiraki
ndi mzinda wa Damasiko
pakuti maso a anthu ndiponso mafuko onse a Israeli
ali pa Yehova—
2 ndiponso mzinda wa Hamati, umene ukuchita malire ndi dzikoli,
komanso pa Turo ndi Sidoni, ngakhale kuti iwo ndi anzeru kwambiri.
3 Ndipo Turo anadzimangira linga;
wadziwunjikira siliva ngati fumbi,
ndi golide ngati zinyalala za m’misewu.
4 Taonani Ambuye adzamulanda chuma chakecho
ndi kuwononga mphamvu zake m’nyanja,
ndipo adzapserera ndi moto.
5 Mzinda wa Asikeloni udzaona zimenezi, n’kuchita mantha;
Gaza adzanjenjemera ndi ululu,
chimodzimodzinso Ekroni, chifukwa chiyembekezo chake chidzatheratu.
Mfumu ya ku Gaza idzaphedwa
ndipo Asikeloni adzakhala opanda anthu.

6 Mu Asidodi mudzakhala mlendo,
ndipo ndidzathetsa kunyada kwa Afilisti.
7 Ndidzachotsa nyama ya magazi m'kamwa mwawo,
chakudya choletsedwa m'mano mwawo.
Amene atsala adzakhala anthu a Mulungu wathu,
adzasanduka atsogoleri mu Yuda,
ndipo Ekroni adzakhala ngati Ayebusi.
8 Koma Ine ndidzalondera Nyumba yanga
ndi kuyiteteza kwa ankhondo osakaza.
Palibenso mdani amene adzagonjetse anthu anga,
pakuti tsopano ndikuwayang'anira.

*Kubwera kwa Mfumu ya Ziyoni*

9 Sangalala kwambiri, iwe mwana wamkazi wa Ziyoni!
Fuwula, mwana wamkazi wa Yerusalemu!
Taona, mfumu yako ikubwera kwa iwe,
yolungama ndi yogonjetsa adani,
yodzichepetsa ndi yokwera pa bulu,
pa mwana wamphongo wa bulu.
10 Ndidzachotsa magaleta ankhondo ku Efereimu
ndi akavalo ankhondo ku Yerusalemu,
ndipo uta wankhondo udzathyoka.
Mfumuyo idzabweretsa mtendere pakati pa mitundu ya anthu.
Ulamuliro wake udzayambira ku nyanja ina mpaka ku nyanja ina,
ndipo kuchokera ku Mtsinje (Yufurate) mpaka ku malekezero a dziko lapansi.
11 Tsono kunena za iwe, chifukwa cha magazi a pangano lako ndi Ine,
ndidzamasula am'ndende ako, ndidzawatulutsa m'dzenje lopanda madzi.
12 Bwererani ku malo anu otetezedwa, inu am'ndende achiyembekezo;
ngakhale tsopano ndikulengeza kuti ndidzakubwezerani zabwino mowirikiza.
13 Ndidzakoka Yuda monga ndimakokera uta wanga,
ndipo Efereimu ndiye muvi wake.
Ndidzadzutsa ana ako iwe Ziyoni,
kulimbana ndi ana ako iwe Grisi,
ndipo ndidzakusandutsa iwe lupanga la munthu wankhondo.

*Kuoneka kwa Yehova*

14 Pamenepo Yehova adzaonekera kwa anthu ake;
mivi yake idzang'anima ngati ching'aning'ani.
Ambuye Yehova adzaliza lipenga;
ndipo adzayenda mu mkuntho wochokera kummwera,
15 ndipo Yehova Wamphamvuzonse adzawateteza.
Iwo adzawononga
ndipo adzagonjetsa ndi miyala ya legeni.
Adzamwa magazi ndi kubangula ngati amwa vinyo;
magazi adzayenderera ngati a m'mbale yowazira magazi
pa ngodya za guwa lansembe.
16 Tsiku limenelo Yehova Mulungu wawo adzawapulumutsa
pakuti anthu ake ali ngati nkhosa.
Adzanyezimira m'dziko lake
ngati miyala yokongola pa chipewa chaufumu.
17 Taonani chikoka ndi kukongola kwawo!

Tirigu adzasangalatsa anyamata,
ndi vinyo watsopano anamwali.

# 10

*Yehova Adzasamalira Yuda*

1 Pemphani mvula kwa Yehova pa nthawi yamphukira;
ndi Yehova amene amapanga mitambo ya mvula.
Iye amagwetsa mivumbi ya mvula kwa anthu,
ndi kumeretsa mbewu za m'munda kwa aliyense.
2 Mafano amayankhula zachinyengo,
owombeza mawula amaona masomphenya abodza;
amafotokoza maloto onama,
amapereka chitonthozo chopandapake.
Choncho anthu amangoyendayenda ngati nkhosa zozunzika
chifukwa chosowa m'busa.

3 "Ine ndawakwiyira kwambiri abusa,
ndipo ndidzalanga atsogoleri;
pakuti Yehova Wamphamvuzonse adzasamalira
nkhosa zake, nyumba ya Yuda,
ndi kuwasandutsa ngati akavalo aulemerero ankhondo.
4 Mu Yuda mudzachokera mwala wapangodya,
mudzachokera chikhomo cha tenti,
mudzachokera uta wankhondo,
mudzachokera mtsogoleri aliyense.
5 Onse pamodzi adzakhala ngati ngwazi zankhondo
zoponda m'matope a m'misewu nthawi yankhondo.
Chifukwa Yehova adzakhala nawo,
adzachita nkhondo ndi kugonjetsa okwera pa akavalo.

6 "Ndidzalimbitsa nyumba ya Yuda
ndi kupulumutsa nyumba ya Yosefe.
Ndidzawabwezeretsa
chifukwa ndawamvera chisoni.
Adzakhala ngati kuti
sindinawakane,
chifukwa ndine Yehova Mulungu wawo
ndipo ndidzawayankha.
7 Aefereimu adzakhala ngati ankhondo amphamvu
adzasangalala ngati anthu amene amwa vinyo.
Ana awo adzaziona zimenezi ndipo adzasangalala;
m'mitima mwawo adzakondwa mwa Ambuye.
8 Ndidzaliza mluzu
ndi kuwasonkhanitsa pamodzi.
Ndithu ndawawombola;
adzachulukana ngati poyamba paja.
9 Ndinawamwaza pakati pa mitundu ina ya anthu,
koma ku mayiko akutaliwo adzandikumbukira.
Iwo pamodzi ndi ana awo adzapulumuka,
ndipo adzabwerera.
10 Ndidzawabweretsa kuchokera ku Igupto
ndipo ndidzawasonkhanitsa kuchokera ku Asiriya.

Ndidzawabwezera ku Giliyadi ndi ku Lebanoni,
mpaka malo woti n'kukhalamo adzatheratu.
11 Adzawoloka nyanja ya masautso;
nyanja yokokoma idzagonja
ndipo madzi onse a mu Nailo adzaphwa.
Kudzikuza kwa Asiriya kudzatha
ndipo ndodo yaufumu ya Igupto idzathyoka.
12 Ndidzalimbitsa iwo mwa Yehova
ndipo adzayenda m'dzina lake,"
akutero Yehova.

# 11

1 Tsekula zitseko zako, iwe Lebanoni,
kuti moto unyeketse mikungudza yako!
2 Lira mwachisoni, iwe mtengo wa payini, pakuti mkungudza wagwa;
mtengo wamphamvu wawonongeka!
Lirani mwachisoni, inu mitengo ya thundu ya Basani;
nkhalango yowirira yadulidwa!
3 Imvani kulira mwachisoni kwa abusa;
msipu wawo wobiriwira wawonongeka!
Imvani kubangula kwa mikango;
nkhalango yowirira ya ku Yorodani yawonongeka!

### *Abusa Awiri*

4 Yehova Mulungu wanga akuti, "Dyetsa nkhosa zimene zikukaphedwa.
5 Amene amagula nkhosazo amazipha ndipo salangidwa. Amene
amazigulitsa amanena kuti, 'Alemekezeke Yehova, ine ndalemera!' Abusa
ake omwe sazimvera chisoni nkhosazo. 6 Pakuti Ine sindidzamveranso
chisoni anthu okhala m'dziko," akutero Yehova. "Ndidzapereka munthu
aliyense m'manja mwa mnansi wake ndi mwa mfumu yake. Iwo
adzazunza dziko, ndipo Ine sindidzawapulumutsa m'manja mwawo."
7 Choncho ine ndinadyetsa nkhosa zokaphedwa, makamaka nkhosa
zoponderezedwa. Pamenepo ndinatenga ndodo ziwiri ndipo yoyamba
ndinayitcha Kukoma mtima ndipo yachiwiri ndinayitcha Umodzi ndipo
ndinadyetsa nkhosazo. 8 Pa mwezi umodzi ndinachotsa abusa atatu.

Abusawo anadana nane, ndipo ndinatopa nawo. 9 Ndinawuza gulu la
nkhosalo kuti, "Sindidzakhalanso m'busa wanu. Imene ikufa, ife, ndipo
imene ikuwonongeka, iwonongeke, zimene zatsala zizidyana."
10 Kenaka ndinatenga ndodo yanga yotchedwa Kukoma mtima ndi
kuyithyola, kuphwanya pangano limene ndinachita ndi mitundu yonse
ya anthu. 11 Linaphwanyidwa tsiku limenelo ndipo nkhosa zosautsidwa
zimene zimandiyang'anitsitsa zinadziwa kuti anali mawu a Yehova.
12 Ndinawawuza kuti, "Ngati mukuganiza kuti zili bwino, patseni
malipiro anga; koma ngati si choncho, sungani malipirowo." Kotero
anandipatsa ndalama zasiliva makumi atatu.
13 Ndipo Yehova anandiwuza kuti, "Ziponye kwa wowumba mbiya,"
mtengo woyenera umene anapereka pondigula Ine! Choncho ndinatenga
ndalama zasiliva makumi atatu ndi kuziponya m'nyumba ya Yehova kwa
wowumba mbiya.
14 Kenaka ndinathyola ndodo yanga yachiwiri yotchedwa Umodzi,
kuthetsa ubale pakati pa Yuda ndi Israeli.

15 Pamenepo Yehova anayankhula nane kuti, “Tenganso zida za m’busa
wopusa. 16 Pakuti ndidzawutsa m’busa m’dzikomo amene sadzasamalira
zotayika, kapena kufunafuna zazing’ono, kapena zovulala, kapena
kudyetsa nkhosa zabwino, koma iye adzadya nyama ya nkhosa zonenepa,
n’kumakukuta ndi ziboda zomwe.
17 “Tsoka kwa m’busa wopandapake,
amene amasiya nkhosa!
Lupanga limukanthe pa mkono wake ndi pa diso lake lakumanja!
Mkono wake ufote kotheratu,
diso lake lamanja lisaonenso.”

# 12

*Kuphedwa kwa Adani a Yerusalemu*

*Ulosi*

1 Uthenga wa Yehova kwa Israeli. Yehova, amene amayala mlengalenga,
amene amayika maziko a dziko lapansi, ndiponso amene amalenga
mzimu wokhala mwa munthu, akunena kuti, 2 “Taonani, ndidzasandutsa
Yerusalemu kukhala chakumwa choledzeretsa chimene chidzasokoneza
mitundu yonse ya anthu yomuzungulira. Yuda adzazingidwa pamodzinso
ndi Yerusalemu. 3 Pa tsiku limenelo, pamene mitundu yonse ya anthu a
dziko lapansi idzasonkhana kulimbana naye, ndidzasandutsa Yerusalemu
thanthwe losatheka kusunthidwa ndi mitundu yonse ya anthu. Onse
oyesa kumusuntha adzadzipweteka. 4 Pa tsiku limenelo kavalo aliyense
ndidzamuchititsa mantha kuti asokonezeke, ndipo wokwerapo wake
ndidzamuchititsa misala,” akutero Yehova. “Ndidzayang’anira nyumba
ya Yuda koma ndidzachititsa khungu akavalo onse a anthu a mitundu ina.
5 Pamenepo atsogoleri a Yuda adzayankhula m’mitima mwawo kuti, ‘Anthu a ku Yerusalemu ndi amphamvu, chifukwa Yehova Wamphamvuzonse
ndiye Mulungu wawo.’

6 “Pa tsiku limenelo ndidzasandutsa atsogoleri a Yuda kukhala ngati
mbawula yotentha pakati pa nkhuni, ngati sakali yoyaka pa mitolo ya
tirigu. Adzatentha mitundu yonse ya anthu yowazungulira, kumanja ndi
kumanzere, koma Yerusalemu sadzasuntha pa malo ake.

7 “Yehova adzapulumutsa malo okhala Yuda poyamba, kuti ulemu wa
nyumba ya Davide ndi wa anthu okhala mu Yerusalemu usapambane
ulemu wa Yuda. 8 Pa tsiku limenelo Yehova adzatchinjiriza onse okhala mu
Yerusalemu, kotero kuti anthu ofowoka kwambiri pakati pawo adzakhala
ngati Davide, ndipo nyumba ya Davide idzakhala ngati Mulungu, ngati
mngelo wa Yehova wowatsogolera. 9 Pa tsiku limenelo ndidzawononga
mitundu yonse yofuna kuthira nkhondo Yerusalemu.

*Kulirira amene Anamulasa*

10 “Ndipo pa nyumba ya Davide ndi pa anthu okhala mu Yerusalemu
ndidzakhuthulirapo mzimu wachisomo ndi wopemphera. Iwo
adzandiyang’ana Ine, amene anamubaya, ndipo adzamulirira kwambiri
monga momwe munthu amalirira mwana wake mmodzi yekhayo,
ndiponso adzamva chisoni kwambiri monga momwe amachitira ndi
mwana woyamba kubadwa. 11 Pa tsiku limenelo mudzakhala kulira
kwakukulu mu Yerusalemu, monga kulira kwa ku Hadadi-Rimoni ku
chigwa cha Megido. 12 Dziko lidzalira kwambiri, fuko lililonse pa lokha,
akazi awo pa okhanso: fuko la Davide pamodzi ndi akazi awo, fuko la

Natani pamodzi ndi akazi awo, 13 nyumba ya Levi pamodzi ndi akazi awo,
fuko la Simei pamodzi ndi akazi awo, 14 ndiponso mafuko onse pamodzi
ndi akazi awo.

# 13

### *Kuyeretsedwa ku Tchimo*

1 "Pa tsiku limenelo nyumba ya Davide adzayitsekulira kasupe wa madzi
pamodzi ndi okhala mu Yerusalemu, kuti awachotsere tchimo lawo ndi
chodetsa chawo.
2 "Pa tsiku limenelo, ndidzafafaniziratu mayina a mafano m'dziko, ndipo
sadzawakumbukiranso," akutero Yehova Wamphamvuzonse. "Ndidza-
chotsa m'dziko aneneri pamodzi ndi mzimu wonyansa. 3 Ndipo ngati wina
aliyense adzafuna kunenera, abambo ndi amayi ake amene anamubereka,
adzamuwuza kuti, 'Uyenera kufa, chifukwa wayankhula bodza m'dzina la
Yehova.' Pamene anenera, makolo ake omwe adzamubaya.
4 "Pa tsiku limenelo mneneri aliyense adzachita manyazi chifukwa cha
masomphenya ake. Sadzavala chovala chake chaubweya ndi cholinga
chonamiza anthu. 5 Iye adzati, 'Sindine mneneri. Ndine mlimi; ndakhala
ndi kulima munda kuyambira ubwana wanga.' 6 Ngati wina adzamufunsa,
'Zilonda zili m'thupi lakoli ndi chiyani?' Iye adzayankha kuti, 'Zilondazi
ndinazilandira m'nyumba ya abwenzi anga.'

### *Kukantha M'busa, Nkhosa Kubalalika*

7 "Dzambatuka iwe lupanga, ukanthe m'busa wanga,
ukanthe munthu amene ali pafupi ndi Ine!"
akutero Yehova Wamphamvuzonse.
Kantha m'busa
ndipo nkhosa zidzabalalika,
ndipo ndidzatambalitsa dzanja langa kuwononga zazing'ono.
8 M'dziko monse, akutero Yehova Wamphamvuzonse,
"zigawo ziwiri mwa zigawo zitatu za anthu zidzakanthidwa ndi kuwonongeka;
koma chigawo chimodzi chidzatsala m'dzikomo.
9 Chigawo chachitatuchi ndidzachiyika pa moto;
ndidzawayeretsa monga momwe amayeretsera siliva
ndi kuwayesa monga momwe amayesera golide.
Adzayitana pa dzina langa
ndipo Ine ndidzawayankha;
Ine ndidzanena kuti, 'Awa ndi anthu anga,'
ndipo iwo adzanena kuti, 'Yehova ndiye Mulungu wathu.' "

# 14

### *Yehova Akubwera ndipo Akulamulira*

1 Taonani tsiku la Yehova likubwera pamene zinthu zimene adani ako
anakulanda azidzagawana iwe ukuona.
2 Ndidzasonkhanitsa anthu a mitundu yonse kuti adzathire nkhondo
Yerusalemu; mzindawu udzalandidwa, nyumba zidzaphwasulidwa, ndipo
akazi adzagwiririridwa. Theka la anthu a mu mzindamu lidzapita ku
ukapolo, koma ena onse otsala mu mzindamu sadzachotsedwa.
3 Pamenepo Yehova adzabwera kudzamenyana ndi mitundu ya anthu
imeneyi, ngati mmene amachitira pa nthawi ya nkhondo. 4 Tsiku limenelo
adzayimirira pa Phiri la Olivi, kummawa kwa Yerusalemu, ndipo Phiri la

Olivilo lidzagawikana pawiri kuyambira kummawa mpaka kumadzulo,
kupanga chigwa chachikulu, kuchititsa kuti theka la phiri lisunthire
kumpoto ndi linalo kummwera. 5 Inu mudzathawa podzera m'chigwa
chapakati pa phirilo, pakuti chidzafika mpaka ku Azeli. Mudzathawa
monga munachitira pa tsiku la chivomerezi nthawi ya Uziya mfumu ya
Yuda. Kenaka Yehova Mulungu wanga adzabwera, pamodzi ndi oyera ake
onse.
6 Tsiku limenelo sipadzakhala kuwala, kuzizira kapena chisanu.
7 Lidzakhala tsiku lapaderadera, silidzakhala usana kapena usiku; tsiku
limeneli akulidziwa ndi Yehova yekha. Ikadzafika nthawi ya madzulo,
kudzakhala kukuwalabe.
8 Tsiku limenelo madzi amoyo adzatuluka mu Yerusalemu, theka lidza-
pita ku nyanja ya kummawa ndipo theka lina ku nyanja ya kumadzulo,
nthawi yachilimwe ndi nthawi yozizira yomwe.
9 Ndipo Yehova adzakhala mfumu pa dziko lonse lapansi. Tsiku limenelo
padzakhala Ambuye mmodzi yekha, ndipo dzina lidzakhala limodzi
lomwelo.
10 Dziko lonse, kuyambira ku Geba mpaka ku Rimoni, kummwera kwa
Yerusalemu, lidzakhala ngati Araba. Koma Yerusalemu adzakwezedwa
ndipo adzakhala pamalo pakepo, kuyambira ku Chipata cha Benjamini
mpaka ku malo amene ali ku Chipata Choyamba, ku Chipata Chapangodya,
ndipo kuyambira ku Nsanja ya Hananeli mpaka ku malo opsinyira mphesa
za mfumu. 11 M'menemo mudzakhala anthu; sadzawonongedwanso.
Yerusalemu adzakhala pa mtendere.
12 Mliri umene Yehova adzakanthire nawo mitundu yonse ya anthu
imene inkamenyana ndi Yerusalemu ndi uwu: Matupi awo adzawola iwo
eni akuyenda, maso awo adzawola ali m'malo mwake, ndipo malilime
awo adzawola ali m'kamwa mwawo. 13 Pa tsiku limenelo Yehova
adzasokoneza anthu akuluakulu. Munthu aliyense adzagwira dzanja la
mnzake, ndi kuyamba kumenyana okhaokha. 14 Yuda nayenso adzachita
nkhondo ku Yerusalemu. Chuma chonse cha anthu a mitundu yozun-
gulira adzachisonkhanitsa pamodzi; golide, siliva ndi zovala zochuluka
kwambiri. 15 Mliri womwewo udzapha akavalo ndi nyulu, ngamira ndi
abulu, pamodzi ndi nyama zonse zokhala ku misasako.
16 Kenaka opulumuka ochokera mwa mitundu yonse ya anthu amene
anathira nkhondo Yerusalemu, azidzapita chaka ndi chaka kukapembedza
Mfumu Yehova Wamphamvuzonse, ndiponso kukachita Chikondwerero
cha Misasa. 17 Ngati mitundu ina ya anthu pa dziko lapansi sidzapita ku
Yerusalemu kukapembedza Mfumu Yehova Wamphamvuzonse, idzakhala
wopanda mvula. 18 Ndipo ngati anthu a ku Igupto sadzapita ndi kukakhala
nawo kumeneko, adzakhala wopanda mvula. Yehova adzabweretsa pa
iwo mliri umene analangira mitundu ina ya anthu imene sinapite ku
Chikondwerero cha Misasa. 19 Chimenechi chidzakhala chilango cha
Igupto ndiponso mitundu ina yonse imene sidzapita ku Chikondwerero
cha Misasa.
20 Pa tsiku limenelo pa maberu a akavalo padzalembedwa mawu oti
WOPATULIKIRA YEHOVA, ndipo miphika ya m'Nyumba ya Yehova idzakhala
yopatulika ngati mbale za ku guwa. 21 M'phika uliwonse ku Yerusalemu
ndi ku Yuda udzakhala wopatulikira Yehova Wamphamvuzonse, ndipo
onse amene adzabwera kudzapereka nsembe adzatenga miphika ina
ndi kuphikiramo. Ndipo nthawi imeneyo simudzakhalanso Akanaani
m'Nyumba ya Yehova Wamphamvuzonse.

# Malaki

1 Uthenga: Mawu a Yehova kwa Israeli kudzera mwa Malaki.

*Ndamukonda Yakobo, Ndamuda Esau*

2 Yehova akuti, "Ine ndakukondani. Koma inu mukufunsa kuti, 'Kodi mwatikonda motani?' "

Yehova akuti, "Kodi Esau sanali m'bale wake wa Yakobo? Komatu Ine
ndinakonda Yakobo, 3 koma ndinamuda Esau, ndipo dziko lake lamapiri
ndalisandutsa chipululu ndipo cholowa chake ndasiyira ankhandwe a m'chipululu."

4 Mwina Edomu n'kunena kuti, "Ngakhale taphwanyidwa, tidzamanganso m'mabwinja."

Koma Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Iwo angathe kumanganso, koma Ine ndidzazigwetsanso. Iwo adzatchedwa dziko loyipa, la anthu
amene Yehova wayipidwa nawo mpaka muyaya. 5 Inu mudzaziona
zimenezi ndi maso anu ndipo mudzati, 'Yehova ndi Wamkulu, ukulu wake umafika ngakhale kunja kwa malire a Israeli!'

*Nsembe Zosayenera*

6 "Mwana amalemekeza abambo ake, ndipo wantchito amaopa abwana ake. Ngati Ine ndine abambo anu, ulemu wanga uli kuti? Ngati ndine mbuye wanu, nanga kundiopa kuli kuti?" Akutero Yehova Wamphamvuzonse.

"Ndinu, inu ansembe, amene mumanyoza dzina langa.

"Komatu mukufunsa kuti, 'Kodi timanyoza dzina lanu bwanji?'

7 "Inu mwanyoza dzina langa popereka chakudya chodetsedwa pa guwa langa lansembe.

"Komatu mukufunsa kuti, 'Kodi ife takunyozani bwanji?'

"Mwandinyoza ponena kuti tebulo la Yehova ndi lonyozeka.
8 Mukamapereka nsembe nyama zosaona, kodi sicholakwa? Mukamapereka nsembe nyama zachilema kapena zodwala, kodi sicholakwa? Kayeseni kuzipereka kwa bwanamkubwa wanu! Kodi akasangalatsidwa nanu? Kodi akazilandira? Akutero Yehova Wamphamvuzonse.

9 "Tsopano tayesani kupempha Mulungu kuti akuchitireni chifundo. Kodi ndi zopereka zotere m'manja mwanu, Iye angakulandireni?" Akutero Yehova Wamphamvuzonse.

10 "Ndikulakalaka mmodzi wa inu akanatseka zitseko za Nyumba ya Mulungu, kuti musayatsemo moto pachabe pa guwa langa lansembe! Ine sindikukondwera nanu," akutero Yehova Wamphamvuzonse, "ndipo Ine
sindidzalandira zopereka za m'manja mwanu. 11 Dzina langa lidzalemekezedwa pakati pa mitundu ya anthu, kuchokera kummawa mpaka kumadzulo. M'malo monse adzapereka nsembe zofukiza ndi zopereka zangwiro m'dzina langa, chifukwa dzina langa lidzakhala lalikulu pakati pa mitundu ya anthu," akutero Yehova Wamphamvuzonse.

12 "Koma inu mumalinyoza ponena kuti tebulo la Ambuye, 'ndi
lodetsedwa,' ndipo chakudya chake, 'n'chonyozeka!' 13 Ndipo inu mumati,
'Ndi zotopetsa zimenezi!' Ndipo mumandinyogodola Ine," akutero Yehova Wamphamvuzonse.

"Pamene inu mubweretsa nyama zakuba, zolumala kapena zodwala ndi kupereka nsembe, kodi Ine ndizilandire kuchokera m'manja mwanu?" Akutero Yehova.
14 "Atembereredwe munthu wachinyengo amene ali ndi nyama yayimuna yabwino m'gulu la ziweto zake ndipo analumbira kuyipereka, koma m'malo mwake n'kupereka nsembe kwa Ambuye nyama yosayenera. Yehova Wamphamvuzonse akuti, 'Pakuti ndine mfumu yayikulu, dzina langa liyenera kuopedwa pakati pa anthu a mitundu yonse.' "

# 2

## *Chenjezo kwa Ansembe*

1 "Tsono chenjezo ili ndi la inu, inu ansembe."
2 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Ngati simumvera, ndipo ngati simulemekeza dzina langa m'mitima mwanu, ndidzakutembererani ndipo madalitso onse munawalandira ndidzawatemberera. Ndithu, ndawatemberera kale, chifukwa simunalemekeze Ine m'mitima mwanu."
3 "Ine ndidzalanga zidzukulu zanu chifukwa cha inu; ndidzakupakani kumaso ndowe za nsembe zanu zachikondwerero, ndipo ndidzakutayani pamodzi ndi ndowezo."
4 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Apo mudzadziwa kuti Ine ndatumiza chenjezoli kuti pangano langa ndi Levi lipitirire.
5 Ine ndinali naye pa pangano, pangano lopatsa moyo ndi mtendere, ndipo ndinamupatsa zimenezi kuti azindiopa, ndipo anandiopadi ndi kulemekeza dzina langa.
6 Pakamwa pake pankatuluka malangizo woona, ndipo pa milomo yake sipanapezeke chinyengo. Iye anayenda nane mwamtendere ndi molungama mtima, ndipo anabweza anthu ambiri m'njira zawo zauchimo.
7 "Pakuti wansembe ayenera kukhala ndi chidziwitso, ndipo anthu ayenera kufunafuna malangizo kuchokera kwa iye, popeza iye ndi mthenga wa Yehova Wamphamvuzonse.
8 Koma inu mwasiya njira yanga ndipo mwapunthwitsa anthu ambiri ndi ziphunzitso zanu; mwayipitsa pangano langa ndi Levi," akutero Yehova Wamphamvuzonse.
9 "Choncho Ine ndachititsa kuti munyozedwe ndi kuchititsidwa manyazi pamaso pa anthu onse, chifukwa simunatsate njira zanga koma mwakhala mukuonetsa kukondera pa nkhani za malamulo."

## *Kusakhulupirika kwa Yuda*

10 Kodi sitili naye Atate mmodzi tonsefe? Kodi anatilenga si Mulungu mmodzi? Chifukwa chiyani tikudetsa pangano la makolo athu posamakhulupirirana wina ndi mnzake?
11 Yuda waleka kukhulupirika. Chinthu chonyansa chachitika mu Israeli ndi mu Yerusalemu: Yuda wayipitsa malo opatulika amene Yehova amawakonda, pokwatira mkazi wopembedza mulungu wachilendo.
12 Ndipo wina aliyense wochita zimenezi, kaya munthuyo ndi wotani, Yehova amuchotse ku banja la Yakobo, ngakhale atabweretsa zopereka kwa Yehova Wamphamvuzonse.
13 China chimene mumachita ndi ichi: Mumakhathamiritsa guwa lansembe la Yehova ndi misozi. Mumalira ndi kufuwula kwambiri chifukwa Iye amakana kuyang'ana nsembe zanu, kapena kulandira mokondwera nsembe za m'manja mwanu.
14 Inu mukufunsa kuti, "Chifukwa chake n'chiyani?" Chifukwa chake n'chakuti Yehova ndi mboni ya pangano limene unachita ndi mkazi wa unyamata wako, chifukwa

sunakhulupirike kwa iye, ngakhale kuti iyeyo ndiye mnzako, ndi mkazi
wako mwapangano.
15 Kodi Yehova sanawalenge iwo ngati munthu mmodzi? Ndi ake
m'thupi ndi mu mzimu. N'chifukwa chiyani ali mmodzi? Chifukwa Iye
amafuna ana opembedza Mulungu. Motero samala moyo wako wauzimu,
ndipo usakhale wosakhulupirika kwa mkazi wa unyamata wako.
16 Yehova Mulungu wa Israeli akuti, "Ndimadana ndi kulekana ukwati.
Ndimadana ndi munthu wochita zankhanza zotere kwa mkazi wake,"
akutero Yehova Wamphamvuzonse.
Choncho tetezani mzimu wanu, ndipo musakhale osakhulupirika.

### *Tsiku la Chiweruzo*

17 Mwamutopetsa Yehova ndi zoyankhula zanu.
Inu mukufunsa kuti, "Kodi tamutopetsa bwanji?"
Mwamutopetsa ponena kuti, "Aliyense amene amachita zoyipa ndi
wabwino pamaso pa Yehova ndipo iye amakondwera naye" kapena
pofunsa kuti, "Ali kuti Mulungu woweruza mwachilungamo?"

## 3

1 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Ine ndidzatuma mthenga wanga
amene adzakonza njira pamaso panga. Kenaka mwadzidzidzi Ambuye
amene mukumufunafuna adzafika ku Nyumba yake. Mthenga wapangano
amene mukumuyembekezera adzabwera."
2 Koma ndani adzatha kupirira pa tsiku la kubwera kwake? Ndani
adzatha kuyima pamene Iye wafika? Pakuti adzakhala ngati moto wa
mmisiri wa pa ng'anjo, kapenanso ngati sopo wa munthu wochapa.
3 Iye adzachita kukhalira pansi ngati mmisiri woyenga ndi woyeretsa
siliva. Iye adzayeretsa Alevi ndi kuwayenga ngati golide ndi siliva.
Pamenepo Yehova adzakhala ndi anthu amene azidzabweretsa zopereka
mwachilungamo, 4 ndipo Yehova adzalandira zopereka za Yuda ndi
Yerusalemu, ngati masiku akale, masiku amakedzana.
5 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Tsono ndidzakuyandikirani kuti
ndikuweruzeni. Mosataya nthawi ndidzanena mawu otsutsa mfiti,
achigololo, a umboni wonama, amene salipira bwino antchito awo, amene
amazunza akazi ndi ana amasiye, amene saweruza alendo mwachilung-
amo, komanso amene sandiopa Ine."

### *Kuba za Mulungu*

6 "Ine ndine Yehova, ndipo sindisintha. Choncho inu zidzukulu za
Yakobo, simunawonongedwe. 7 Kuyambira nthawi ya makolo anu
mwakhala mukuphwanya malamulo anga ndipo simunawatsatire. Bw-
ererani kwa Ine, ndipo Ine ndidzabwerera kwa inu," akutero Yehova
Wamphamvuzonse.
"Koma inu mukufunsa kuti, 'Tibwerere motani kwa Yehova?'
8 "Kodi munthu angathe kuba za Mulungu? Komatu inu mumandibera.
"Koma inu mukufunsa kuti, 'Kodi timakuberani motani?'
"Pa zakhumi ndi pa zopereka. 9 Mtundu wanu wonse ndinu otem-
bereredwa, chifukwa mukundibera. 10 Bweretsani chakhumi chathunthu
ku nyumba yosungira, kuti mukhale chakudya m'nyumba mwanga."
Akutero Yehova Wamphamvuzonse, "Tandiyesani, ndipo muone ngati
sindidzatsekula zipata zakumwamba, ndi kukugwetserani madalitso ochu-
luka amene mudzasowe malo owayikamo. 11 Ndidzaletsa tizirombo kuti
tisawononge mbewu zanu, ndipo mpesa wa m'minda mwanu zipatso

zake sizidzayoyoka," akutero Yehova Wamphamvuzonse. 12 "Motero
anthu amitundu yonse adzakutchulani odala, pakuti dziko lanu lidzakhala
lokondweretsa," akutero Yehova Wamphamvuzonse.

13 Yehova akuti, "Mwayankhula mawu owawa onena za Ine.

"Komabe inu mukufunsa kuti, 'Kodi tanena chiyani chotsutsana nanu?'

14 "Mwanena kuti, 'Kutumikira Mulungu n'kosapindulitsa. Kodi
timapindulanji pochita zofuna zake, ndi kumayenda ngati anamfedwa
pamaso pa Yehova Wamphamvuzonse? 15 Koma tsono ife timati anthu
odzikuza ndiye odalitsika. Kunena zoona anthu oyipa ndiye amapeza
bwino, ngakhale amene amanyoza Mulungu amapulumuka.' "

16 Ndipo woopa Yehova anayamba kukambirana, ndipo Yehova
anamvetsera. Buku la chikumbutso linalembedwa pamaso pake, lonena
za amene amaopa Yehova ndi kulemekeza dzina lake.

17 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Anthu amenewo adzakhala anga,
tsiku limene Ine ndidzachita izi, adzakhala angaanga. Ndidzawaleka
osawalanga monga mmene munthu amachitira chifundo mwana wake
amene amamutumikira. 18 Pamenepo mudzaonanso kusiyana pakati pa
anthu olungama ndi oyipa, pakati pa amene amatumikira Mulungu ndi
amene satumikira Mulungu."

# 4

*Tsiku la Yehova*

1 Yehova Wamphamvuzonse akuti, "Ndithu tsiku likubwera; lidzayaka
ngati ng'anjo. Anthu onse odzikuza, ndi aliyense ochita zoyipa adzapsa
ngati chiputu, ndipo pa tsiku limene likubweralo adzapserera ndi moto.
Sipadzatsalira muzu kapena nthambi. 2 Koma inu amene mumaopa dzina
langa, dzuwa lachilungamo lidzakutulukirani lili ndi kuwala kokuchirit-
sani. Ndipo inu mudzatuluka ndi kulumphalumpha ngati ana ang'ombe
amene atulutsidwa m'khola. 3 Tsiku limenelo inu mudzapondereza anthu
oyipa; adzakhala phulusa ku mapazi anu pa tsiku limene Ine ndidzachite
zinthu zimenezi," akutero Yehova Wamphamvuzonse.

4 Kumbukirani zophunzitsa za mtumiki wanga Mose, malamulo ndi
malangizo amene ndinamupatsa pa Horebu kuti awuze Aisraeli onse.

5 "Taonani, ndidzakutumizirani mneneri Eliya lisanafike tsiku lalikulu
ndi loopsa la Yehova. 6 Iye adzabweza mitima ya makolo kwa ana awo,
ndi mitima ya ana kwa makolo awo. Kupanda kutero ndidzabwera
kudzakantha dziko lanu ndi temberero."

# UTHENGA WABWINO WA YESU KHRISTU WOLEMBEDWA NDI MATEYU

*Makolo a Yesu Khristu Monga mwa Thupi*

1 Buku lofotokoza za m'bado wa Yesu Khristu mwana wa Davide, mwana wa Abrahamu:

2 Abrahamu anabereka Isake,
Isake anabereka Yakobo,
Yakobo anabereka Yuda ndi abale ake.
3 Yuda anabereka Perezi ndi Zara, amene amayi awo anali Tamara.
Perezi anabereka Hezironi,
Hezironi anabereka Aramu.
4 Aramu anabereka Aminadabu,
Aminadabu anabereka Naasoni,
Naasoni anabereka Salimoni.
5 Salimoni anabereka Bowazi amene amayi ake anali Rahabe,
Bowazi anabereka Obedi amene amayi ake anali Rute,
Obedi anabereka Yese.
6 Yese anabereka Mfumu Davide.

Ndipo Davide anabereka Solomoni, amene amayi ake anali mkazi wa Uriya.
7 Solomoni anabereka Rehabiamu,
Rehabiamu anabereka Abiya,
Abiya anabereka Asa,
8 Asa anabereka Yehosafati,
Yehosafati anabereka Yoramu,
Yoramu anabereka Uziya.
9 Uziya anabereka Yotamu,
Yotamu anabereka Ahazi,
Ahazi anabereka Hezekiya.
10 Hezekiya anabereka Manase,
Manase anabereka Amoni,
Amoni anabereka Yosiya.
11 Yosiya anali atabala Yekoniya ndi abale ake pamene Ayuda anatengedwa ukapolo kupita ku Babuloni.

12 Ali ku ukapolo ku Babuloni,
Yekoniya anabereka Salatieli,
Salatieli anabereka Zerubabeli.
13 Zerubabeli anabereka Abiudi,
Abiudi anabereka Eliakimu,
Eliakimu anabereka Azoro.
14 Azoro anabereka Zadoki,
Zadoki anabereka Akimu,
Akimu anabereka Eliudi.
15 Eliudi anabereka Eliezara,
Eliezara anabereka Matani,
Matani anabereka Yakobo.

16 Yakobo anabereka Yosefe, mwamuna wa Mariya. Mariyayu ndiye anabereka Yesu wotchedwa Khristu.

17 Kuyambira pa Abrahamu mpaka pa Davide, pali mibado khumi ndi
inayi. Ndipo kuyambira pa Davide mpaka pamene Ayuda anatengedwa kupita ku ukapolo ku Babuloni, pali mibado khumi ndi inayi. Ndiponso kuyambira nthawi ya ukapolo ku Babuloni mpaka pamene Khristu anabadwa, palinso mibado khumi ndi inayi.

*Kubadwa kwa Yesu Khristu*

18 Kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Amayi ake, Mariya,
anapalidwa ubwenzi ndi Yosefe, koma asanagone malo amodzi, anapezeka
ali woyembekezera mwana mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. 19 Popeza
Yosefe mwamuna wake anali munthu wolungama, sanafune kumuchititsa manyazi pomuleka poyera. Choncho anaganiza zomuleka mosaonetsera.
20 Koma akuganiza zimenezi, taonani, mngelo wa Ambuye anamuonek-
era m'maloto nati, "Yosefe mwana wa Davide, usaope kumutenga Mariya kukhala mkazi wako, chifukwa mwana akuyembekezerayo ndi
wochokera kwa Mzimu Woyera. 21 Ndipo adzabala mwana wamwamuna,
udzamutcha dzina lake Yesu; pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo."
22 Zonsezi zinachitika kukwaniritsa zimene Ambuye ananena mwa
mneneri kuti, 23 "Onani namwali adzakhala woyembekezera ndipo
adzabala mwana wamwamuna, ndipo mwanayo adzamutcha Imanueli," kutanthauza kuti, "Mulungu ali nafe."
24 Yosefe atadzuka, anachita zomwe mngelo wa Ambuye uja anamula-
mulira. Iye anamutenga Mariya kukhala mkazi wake. 25 Koma sanagone
malo amodzi mpaka mwanayo atabadwa ndipo anamutcha dzina lake Yesu.

# 2

*Anzeru a Kummawa*

1 Atabadwa Yesu m'Betelehemu wa ku Yudeya, m'nthawi ya mfumu
Herode, Anzeru a kummawa anabwera ku Yerusalemu 2 nafunsa kuti,
"Ali kuti amene wabadwa kukhala mfumu ya Ayuda? Chifukwa tinaona nyenyezi yake kummawa ndipo tabwera kudzamupembedza."
3 Mfumu Herode atamva zimenezi, anavutika mu mtima kwambiri
pamodzi ndi anthu onse a mu Yerusalemu. 4 Ndipo anayitanitsa anthu
onse, akulu ansembe ndi aphunzitsi amalamulo nawafunsa kuti, "Kodi
Khristu adzabadwira kuti?" 5 Ndipo anamuyankha kuti, "Ku Betelehemu
wa ku Yudeya chifukwa izi ndi zimene mneneri analemba kuti,
6 " 'Koma iwe Betelehemu, chigawo cha Yudeya,
sindiwe wamng'onong'ono mwa olamulira a Yudeya;
pakuti otsogolera adzachokera mwa iwe,
amene adzaweta anthu anga Aisraeli.' "
7 Pomwepo Herode anawayitanira mseri Anzeruwo nawafunsitsa
nthawi yeniyeni yomwe nyenyeziyo inaoneka. 8 Ndipo anawatumiza ku
Betelehemu nawawuza kuti, "Pitani mukafufuze za mwanayo mosamalitsa. Ndipo mukamupeza mudzandiwuze kuti inenso ndikamupembedze."
9 Atamva mawu a mfumu, ananyamuka ulendo wawo, ndipo taonani nyenyezi anayiona kummawa ija, inawatsogolera mpaka inayima
pamwamba pa nyumba yomwe munali mwanayo. 10 Pamene iwo anaona

nyenyeziyo, anasangalala kwambiri. 11 Pofika ku nyumbayo, anaona
mwanayo pamodzi ndi amayi ake Mariya, ndipo anagwada namulambira
Iye. Pomwepo anamasula chuma chawo ndi kupereka mphatso zawo za
ndalama zagolide, lubani ndi mure. 12 Ndipo atachenjezedwa m'maloto
kuti asapitenso kwa Herode, anabwerera ku dziko la kwawo podzera njira
ina.

### *Athawira ku Igupto*

13 Atachoka, taonani mngelo wa Ambuye anaonekera kwa Yosefe
m'maloto nati, "Tadzuka, tenga mwanayo pamodzi ndi amayi ake ndipo
muthawire ku Igupto. Mukakhale kumeneko mpaka nditakuwuza pakuti
Herode adzafunafuna mwanayo kuti amuphe." 14 Atadzuka, Yosefe
anatenga mwanayo ndi amayi ake usiku omwewo napita ku Igupto,
15 nakhala kumeneko mpaka Herode atamwalira. Ndipo zinakwanirit-
sidwa zomwe ananena Ambuye mwa mneneri kuti, "Ndinayitana mwana
wanga kuti atuluke mu Igupto."

### *Kuphedwa kwa Ana m'Betelehemu*

16 Herode atazindikira kuti Anzeruwo anamupusitsa, anakwiya
kwambiri. Ndipo anatumiza anthu kukapha ana onse aamuna a
m'Betelehemu ndi midzi yozungulira amene anali a zaka ziwiri kapena
zocheperapo, molingana ndi nthawi imene Anzeruwo anamuwuza.
17 Pamenepo, zimene ananena mneneri Yeremiya zinakwaniritsidwa:
18 "Kulira kukumveka ku Rama,
kubuma ndi kulira kwakukulu,
Rakele akulirira ana ake;
sakutonthozeka,
chifukwa ana akewo palibe."

### *Abwerera ku Nazareti*

19 Atamwalira Herode, mngelo wa Ambuye anaonekera kwa Yosefe
m'maloto ku Igupto 20 nanena kuti, "Nyamuka, tenga mwanayo ndi amayi
ake ndipo mupite ku dziko la Israeli, popeza amene anafuna moyo wa
mwanayo anamwalira."
21 Tsono Yosefe atadzuka anatenga mwanayo ndi amayi ake kupita ku
dziko la Israeli. 22 Koma atamva kuti Arikelao akulamulira mu Yudeya
m'malo mwa abambo ake, Herode, anaopa kupitako. Atachenjezedwa
m'maloto, anapita ku Galileya, 23 ndipo anakakhazikika mu mzinda wa
Nazareti. Pamenepo zinakwaniritsidwa zonenedwa ndi aneneri kuti,
"Adzatchedwa Mnazareti."

## 3

### *Yohane M'batizi*

1 M'masiku amenewo, Yohane M'batizi anadza nalalikira m'chipululu
cha Yudeya 2 kuti, "Tembenukani mtima chifukwa ufumu wakumwamba
wayandikira." 3 Uyu ndi amene mneneri Yesaya ananena za iye kuti,
"Mawu a wofuwula m'chipululu,
'Konzani njira ya Ambuye,
wongolani njira zake.' "
4 Zovala za Yohane zinali zopangidwa ndi ubweya wa ngamira, ndipo
amamangira lamba wachikopa m'chiwuno mwake. Chakudya chake
chinali dzombe ndi uchi wa kuthengo. 5 Anthu ankapita kwa iye
kuchokera ku Yerusalemu ndi ku Yudeya konse ndi ku madera onse a

Yorodani. 6 Ndipo akavomereza machimo awo ankabatizidwa mu mtsinje
wa Yorodani.

7 Koma iye ataona Afarisi ndi Asaduki ambiri akubwera kumene ankaba-
tiza, anawawuza kuti, "Ana a njoka inu! Ndani anakuchenjezani kuthawa
mkwiyo umene ukubwera? 8 Onetsani chipatso cha kutembenuka mtima.
9 Ndipo musaganize ndi kunena mwa inu nokha kuti, 'Tili nawo abambo
athu Abrahamu.' Ndinena kwa inu kuti Mulungu akhoza kusandutsa
miyala iyi kukhala ana a Abrahamu. 10 Tikukamba pano nkhwangwa
yayikidwa kale pa mizu ya mitengo, ndipo mtengo umene subala chipatso
chabwino udulidwa ndi kuponyedwa pa moto.

11 "Ine ndikubatizani ndi madzi kusonyeza kutembenuka mtima. Koma
pambuyo panga akubwera wina amene ali ndi mphamvu kuposa ine,
amene sindiyenera kunyamula nsapato zake. Iyeyu adzakubatizani
ndi Mzimu Woyera ndi moto. 12 M'dzanja lake muli chopetera ndipo
adzayeretsa popunthirapo pake nadzathira tirigu wake m'nkhokwe ndi
kutentha zotsalira zonse ndi moto wosazima."

### *Kubatizidwa kwa Yesu*

13 Pamenepo Yesu anabwera kuchokera ku Galileya kudzabatizidwa ndi
Yohane mu mtsinje wa Yorodani. 14 Koma Yohane anayesetsa kumukanira
nati, "Ndiyenera kubatizidwa ndi Inu, bwanji Inu mubwera kwa ine?"

15 Yesu anayankha kuti, "Zibatero tsopano, ndi koyenera kwa ife kuchita
zimenezi kukwaniritsa chilungamo chonse." Ndipo Yohane anavomera.

16 Yesu atangobatizidwa, nthawi yomweyo potuluka m'madzi,
kumwamba kunatsekuka ndipo taonani, Mzimu wa Mulungu anatsika
ngati nkhunda natera pa Iye. 17 Ndipo mawu anamveka kuchokera
kumwamba kuti, "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa amene
ndikondwera naye."

## 4

### *Yesu Ayesedwa M'chipululu*

1 Pambuyo pake Yesu anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera kupita ku
chipululu kukayesedwa ndi mdierekezi. 2 Ndipo atasala kudya masiku
makumi anayi usana ndi usiku, anamva njala. 3 Woyesayo anadza kwa
Iye nati, "Ngati ndinu mwana wa Mulungu, sandutsani miyala iyi kuti
ikhale buledi."

4 Yesu anayankha kuti, "Zalembedwa, 'Munthu sadzakhala ndi moyo
ndi chakudya chokha, koma ndi mawu aliwonse ochokera m'kamwa mwa
Mulungu.' "

5 Pamenepo mdierekezi anapita naye ku mzinda woyera namuyimiritsa
pamwamba penipeni pa Nyumba ya Mulungu. 6 Ndipo anati, "Ngati ndinu
Mwana wa Mulungu, dziponyeni nokha pansi. Pakuti kwalembedwa:

" 'Adzalamulira angelo ake za iwe,
ndipo adzakunyamula ndi manja awo
kuti phazi lako lisagunde pa mwala.' "

7 Yesu anamuyankha kuti, "Kwalembedwanso: 'Musamuyese Yehova
Mulungu wanu.' "

8 Kenaka mdierekezi anamutengera Yesu ku phiri lalitali kwambiri
namuonetsa maufumu onse a dziko lapansi ndi ulemerero wawo. 9 Ndipo
anati kwa Iye, "Zonsezi ndidzakupatsani ngati mutandiweramira ndi
kundipembedza ine."

10 Yesu anati kwa iye, “Choka Satana! Zalembedwa, ‘Pembedza Yehova
Mulungu wako ndi kumutumikira Iye yekha.’ ”
11 Pamenepo mdierekezi anamusiya ndipo angelo anamutumikira Iye.

### *Yesu Ayamba Kulalikira*

12 Yesu atamva kuti Yohane anamutsekera m’ndende, anabwerera
ku Galileya. 13 Ndipo atachoka ku Nazareti anapita ku Kaperenawo
ndi kukhala m’mbali mwa nyanja, m’dera la Zebuloni ndi Nafutali;
14 pokwaniritsa zimene zinanenedwa kudzera mwa mneneri Yesaya kuti,
15 “Dziko la Zebuloni ndi dziko la Nafutali,
njira ya ku nyanja, kutsidya lija la Yorodani,
Galileya wa anthu a mitundu ina,
16 anthu okhala mu mdima
awona kuwala kwakukulu;
ndi kwa iwo okhala m’dziko la mthunzi wa imfa
kuwunika kwawafikira.”
17 Kuyambira nthawi imeneyo, Yesu anayamba kulalikira nati, “Tembe-
nukani mtima ufumu wakumwamba wayandikira.”

### *Yesu Ayitana Ophunzira ake Oyamba*

18 Pamene Yesu ankayenda m’mbali mwa nyanja ya Galileya, anaona
abale awiri, Simoni wotchedwa Petro ndi m’bale wake Andreya akuponya
khoka m’nyanja popeza anali asodzi. 19 Yesu anati, “Bwerani, tsateni Ine
ndipo ndidzakusandutsani asodzi a anthu.” 20 Nthawi yomweyo anasiya
makoka awo namutsata Iye.
21 Atapita patsogolo, anaona abale ena awiri, Yakobo ndi m’bale wake
Yohane ana a Zebedayo. Iwowa anali m’bwato ndi abambo awo, Zebedayo,
akukonza makoka awo ndipo Yesu anawayitana. 22 Nthawi yomweyo
anasiya bwato ndi abambo awo namutsata Iye.

### *Yesu Achiritsa Odwala*

23 Yesu anayendayenda mu Galileya kuphunzitsa m’masunagoge awo,
nalalikira Uthenga Wabwino wa ufumu ndi kuchiritsa matenda onse
pakati pa anthu. 24 Mbiri yake yonse inawanda ku Siriya konse
ndipo anthu anabweretsa kwa Iye onse amene anali odwala nthenda
zosiyanasiyana, womva maululu aakulu, ogwidwa ndi ziwanda, odwala
matenda akugwa ndi olumala ndipo Iye anawachiritsa. 25 Magulu ambiri
a anthu anachokera ku Galileya, Dekapoli, Yerusalemu, Yudeya ndi ku
madera a kutsidya la mtsinje wa Yorodani namutsata Iye.

## 5

### *Chiphunzitso cha pa Phiri*

1 Iye ataona anthu ambiri, anakwera pa phiri nakhala pansi. Ndipo
ophunzira ake anabwera kwa Iye, 2 ndipo anayamba kuwaphunzitsa kuti,
3 “Odala ndi amene ali osauka mu mzimu,
chifukwa ufumu wakumwamba ndi wawo.
4 Odala ndi amene ali achisoni,
chifukwa adzatonthozedwa.
5 Odala ndi amene ali ofatsa,
chifukwa adzalandira dziko lapansi.
6 Odala ndi amene akumva njala ndi ludzu la chilungamo,
chifukwa adzakhutitsidwa.

7 Odala ndi amene ali ndi chifundo,
chifukwa adzawachitira chifundo.
8 Odala ndi amene ali oyera mtima,
chifukwa adzaona Mulungu.
9 Ndi odala amene amabweretsa mtendere,
chifukwa adzatchedwa ana a Mulungu.
10 Odala ndi amene akuzunzidwa chifukwa cha chilungamo,
pakuti ufumu wakumwamba ndi wawo."

11 "Inu ndinu odala anthu akamakunyozani, kukuzunzani,
kukunenerani zoyipa zilizonse ndi kukunamizirani chifukwa cha Ine.
12 Sangalalani, kondwerani chifukwa mphotho yanu ndi yayikulu
kumwamba, chifukwa moterenso ndi mmene anazunzira aneneri inu
musanabadwe.

### *Mchere ndi Kuwunika*

13 "Inu ndinu mchere wa dziko lapansi. Koma ngati mcherewo
usukuluka, adzawukometsanso ndi chiyani? Ulibenso ntchito koma
kungowutaya kunja, anthu nawuponda.

14 "Inu ndinu kuwunika kwa dziko lapansi. Mzinda wa pa phiri sungathe
kubisika. 15 Anthu sayatsa nyale ndikuyivundikira ndi mbiya, m'malo
mwake amayika poonekera ndipo imawunikira onse m'nyumbamo.
16 Momwemonso kuwunika kwanu kuwale pamaso pa anthu kuti aone
ntchito zanu zabwino ndi kulemekeza Atate anu akumwamba.

### *Kukwaniritsa Malamulo*

17 "Musaganize kuti ndinadza kudzathetsa malamulo kapena zonena
za aneneri; sindinabwere kudzathetsa koma kukwaniritsa. 18 Ine
ndikukuwuzani zoonadi kuti, kufikira kutha kwa thambo ndi dziko
lapansi, chilichonse chimene chinalembedwa m'malamulo, ngakhale
kalemba kakang'onong'ono, chidzakwaniritsidwa. 19 Chifukwa chake
aliyense amene aphwanya limodzi la malamulowa ngakhale lal-
ing'onong'ono ndi kuphunzitsa ena kuti achite chimodzimodzi, adzakhala
wotsirizira mu ufumu wakumwamba, koma aliyense amene achita ndi ku-
phunzitsa malamulo awa adzakhala wamkulu mu ufumu wakumwamba.
20 Chifukwa chake ndikuwuzani kuti ngati chilungamo chanu sichiposa
cha Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo, zoonadi, simudzalowa mu ufumu
wakumwamba.

### *Zokhudza Kupha*

21 "Munamva kuti kunanenedwa kwa anthu kale kuti, 'Usaphe
ndipo kuti aliyense amene apha munthu adzaweruzidwa.' 22 Koma
Ine ndikukuwuzani kuti aliyense wokwiyira m'bale wake adzapezeka
wolakwa ku bwalo la milandu. Ndiponso aliyense amene wonena m'bale
wake kuti, 'Ndiwe wopanda phindu,' adzapezeka wolakwa ku bwalo la
milandu lalikulu. Ndipo aliyense amene anganene mnzake 'wopanda-
pake' adzatengeredwa ku bwalo la milandu. Ndiponso aliyense amene
angamunene mnzake kuti, 'Chitsiru iwe,' adzaponyedwa ku gehena.

23 "N'chifukwa chake, pamene ukupereka chopereka chako pa guwa
lansembe ndipo nthawi yomweyo ukumbukira kuti m'bale wako ali
nawe chifukwa, 24 usiye choperekacho pa guwa lansembepo, choyamba
pita kayanjane ndi m'bale wako; ukatero bwera kudzapereka chopereka
chakocho.

25 “Fulumira kuyanjana ndi mnzako amene unamulakwira nthawi ya
milandu isanafike chifukwa angakupereke kwa oweruza amene angaku-
pereke kwa mlonda ndipo mlondayo angakutsekere m’ndende. 26 Zoonadi,
Ine ndikukuwuza kuti sudzatuluka m’ndende mpaka utalipira zonse.

*Zokhudza Chigololo*

27 “Munamva kuti kunanenedwa kuti, ‘Usachite chigololo.’ 28 Koma
Ine ndikuwuzani kuti aliyense woyang’ana mkazi momusirira wachita
naye kale chigololo mu mtima mwake. 29 Ngati diso lako lakumanja
likuchimwitsa, ulichotse ndi kulitaya. Pakuti n’kwabwino kwa iwe kutaya
chiwalo chimodzi cha thupi lako, kusiyana ndi kuti thupi lonse liponyedwe
m’gehena. 30 Ndipo ngati dzanja lako lamanja likuchimwitsa, ulidule ndi
kulitaya. Pakuti n’kwabwino kwa iwe kutaya chiwalo chimodzi cha thupi
lako, kusiyana ndi kuti thupi lonse liponyedwe m’gehena.

*Zokhudza Kusudzula Mkazi*

31 “Ananena kuti, ‘Aliyense wosudzula mkazi wake ayenera amupatse
kalata ya chisudzulo.’ 32 Koma Ine ndikukuwuzani kuti aliyense amene
asudzula mkazi wake pa chifukwa china chilichonse osati chifukwa cha
chiwerewere, akumuchititsa mkaziyo chigololo ndipo aliyense wokwatira
mkaziyo, akuchitanso chigololo.

*Malonjezo*

33 “Munamvanso kuti kunanenedwa kwa anthu akale kuti, ‘Musaph-
wanye lonjezo; koma sungani malonjezo anu amene mwachita kwa
Yehova.’ 34 Koma ndikuwuzani kuti musalumbire ndi pang’ono pomwe
kutchula kumwamba chifukwa kuli mpando waufumu wa Mulungu.
35 Kapena kutchula dziko lapansi, chifukwa ndi chopondapo mapazi ake;
kapena kutchula Yerusalemu, chifukwa ndi mzinda wa mfumu yayikulu.
36 Ndipo musalumbire ndi mutu wanu chifukwa simungathe kuyeretsa
ngakhale kudetsa tsitsi limodzi. 37 Koma ‘Inde’ wanu akhaledi ‘Inde’
kapena ‘Ayi’ wanu akhaledi ‘Ayi,’ chilichonse choposera apa, chichokera
kwa woyipayo.

*Za Kubwezera Choyipa*

38 “Munamva kuti, ‘Diso kulipira diso ndi dzino kulipira dzino.’ 39 Koma
ndikuwuzani kuti musamukanize munthu woyipa, akakumenya patsaya
mupatseni tsaya linalo. 40 Ndipo ngati wina afuna kukuzenga mlandu
kuti akulande malaya ako, umupatsenso mkanjo wako. 41 Ngati wina
akukakamiza kuti uyende naye mtunda umodzi, iwe uyende naye mitunda
iwiri. 42 Wina akakupempha kanthu umupatse, ndipo wofuna kubwereka
usamukanize.

*Kukonda Adani*

43 “Munamva kuti, ‘Konda mnansi wako ndi kudana ndi mdani wako.’
44 Koma Ine ndikuwuzani kuti, ‘Kondani adani anu ndi kuwapempherera
okuzunzani 45 kuti mukhale ana a Atate anu akumwamba, amene awalitsa
dzuwa lake pa oyipa ndi pa abwino, nagwetsa mvula pa olungama ndi
pa osalungama.’ 46 Ngati mukonda amene akukondani inu, mudzapeza
mphotho yanji? Kodi ngakhale amisonkho sachita chimodzimodzi?
47 Ndipo ngati inu mupatsa moni abale anu okhaokha mukuchita
chiyani choposa ena? Kodi ngakhale akunja sachita chimodzimodzi?
48 N’chifukwa chake, inu khalani angwiro monga Atate anu akumwamba
ali wangwiro.”

# 6

*Zopereka Zachifundo*

1 “Samalani kuti musachite ntchito zanu zolungama pamaso pa anthu
kuti akuoneni. Popeza ngati mutero simudzalandira mphotho yochokera
kwa Atate anu akumwamba.

2 “Pamene mupereka zachifundo, musachite modzionetsera monga
amachita achiphamaso m’masunagoge ndi pa misewu kuti atamidwe ndi
anthu. Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti iwowo alandiriratu mphotho yawo
yonse. 3 Koma pamene mupereka zachifundo, dzanja lanu lamanzere
lisadziwe chimene dzanja lanu lamanja likuchita, 4 kotero kuti kupereka
kwanu kukhale mwachinsinsi. Ndipo Atate anu amene amaona zochitika
mwachinsinsi, adzakupatsani mphotho.

*Za Kupemphera*

5 “Pamene mupemphera, musakhale ngati achiphamaso, chifukwa iwo
amakonda kupemphera choyimirira m’masunagoge ndi pa mphambano
za m’misewu kuti anthu awaone. Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti iwo
alandiriratu mphotho yawo yonse. 6 Koma pamene mupemphera, lowani
m’chipinda chanu cham’kati, ndi kutseka chitseko ndipo mupemphere
kwa Atate anu amene saoneka. Ndipo Atate anu, amene amaona zochitika
mseri, adzakupatsani mphotho. 7 Ndipo pamene mukupemphera, musam-
abwerezabwereza monga akunja, pakuti iwo amaganiza kuti adzamveka
chifukwa chochulutsa mawu. 8 Musakhale ngati iwo chifukwa Atate anu
amadziwa zimene musowa musanapemphe.

9 “Chifukwa chake pempherani motere:

“ ‘Atate athu akumwamba,
dzina lanu lilemekezedwe,
10 Ufumu wanu ubwere,
chifuniro chanu chichitike
pansi pano monga kumwamba.
11 Mutipatse chakudya chathu chalero.
12 Mutikhululukire mangawa athu,
monga ifenso tawakhululukira amangawa athu.
13 Ndipo musatitengere kokatiyesa;
koma mutipulumutse kwa woyipayo.’

14 Ngati inu mukhululukira anthu pamene akuchimwirani, Atate anu
akumwamba adzakukhululukirani. 15 Koma ngati inu simukhululukira
anthu zolakwa zawo, Atate anunso sadzakukhululukirani machimo anu.

*Kusala Kudya*

16 “Pamene mukusala kudya, musaonetse nkhope yachisoni monga
achita achiphamaso, pakuti iwo amasintha nkhope zawo kuonetsa anthu
kuti akusala kudya. Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti iwo alandiriratu
mphotho yawo yonse. 17 Koma pamene ukusala kudya, samba m’maso
nudzole mafuta kumutu, 18 kuti usaonekere kwa anthu kuti ukusala kudya
koma kwa Atate ako ali mseri; ndipo Atate ako amene amaona za mseri
adzakupatsa mphotho.

*Za Chuma cha Kumwamba*

19 “Musadziwunjikire chuma pa dziko lapansi, pamene njenjete ndi
dzimbiri zimawononga ndi pamene mbala zimathyola ndi kuba. 20 Koma

mudziwunjikire chuma kumwamba kumene njenjete ndi dzimbiri sizi-
wononga ndipo mbala sizithyola ndi kuba. 21 Pakuti kumene kuli chuma
chako, mtima wako udzakhala komweko.

### *Diso Nyale ya Thupi*

22 "Diso ndi nyale ya thupi. Ngati maso ako ali bwino, thupi lako lonse
lidzakhala m'kuwala. 23 Koma ngati maso ako sali bwino, thupi lako lonse
lidzakhala mu mdima. Koma ngati kuwala kuli mwa iwe ndi mdima, ndiye
kuti mdimawo ndi waukulu bwanji!

24 "Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa ambuye awiri. Pakuti
pena adzamuda mmodzi ndi kukonda winayo kapena adzagwira ntchito
mokhulupirika kwa mmodzi, nadzanyoza winayo. Simungathe kukhala
kapolo wa Mulungu ndi wa chuma pa nthawi imodzi.

### *Musade Nkhawa*

25 "N'chifukwa chake ndikuwuzani kuti musadere nkhawa za moyo
wanu kuti mudzadya chiyani kapena mudzamwa chiyani; kapenanso za
thupi lanu kuti mudzavala chiyani. Kodi moyo suposa chakudya? Kodi
thupi siliposa zovala? 26 Onani mbalame zamlengalenga sizifesa kapena
kukolola kapena kusunga m'nkhokwe komabe Atate anu akumwamba
amazidyetsa. Kodi inu simuziposa kwambiri? 27 Kodi ndani wa inu
podandaula angathe kuwonjeza ora limodzi pa moyo wake?

28 "Ndipo bwanji inu mudera nkhawa za zovala? Onani makulidwe
a maluwa akutchire. Sagwira ntchito kapena kuwomba nsalu.
29 Ndikukuwuzani kuti angakhale Solomoni mu ulemerero wake sanavale
mofanana ndi limodzi la maluwa amenewa. 30 Ngati umu ndi mmene
Mulungu avekera udzu wa kutchire umene ulipo lero ndipo mawa up-
onyedwa ku moto, kodi sadzakuvekani koposa? Aa! Inu a chikhulupiriro
chochepa! 31 Chifukwa chake musadere nkhawa ndi kuti, 'Tidzadya
chiyani?' kapena 'Tidzamwa chiyani?' kapena 'Tidzavala chiyani?'
32 Pakuti anthu akunja amazifuna zinthu zonsezi ndipo Atate anu
akumwamba adziwa kuti musowa zimenezi. 33 Koma muyambe mwafuna
ufumu wake ndi chilungamo chake ndipo zinthu zonsezi zidzapatsidwa
kwa inu. 34 Chifukwa chake musadere nkhawa ndi za mawa, popeza tsiku
lililonse lili ndi zovuta zake zokwanira.

## 7

### *Za Kuweruza Ena*

1 "Musaweruze ena, kuti inunso mungadzaweruzidwe. 2 Pakuti momwe
inu muweruzira ena, inunso mudzaweruzidwa chimodzimodzi, muyeso
umene muyesera ena inunso mudzayesedwa ndi womwewo.

3 "Chifukwa chiyani iwe uyang'ana kachitsotso ka m'diso la m'bale wako
koma susamalira chimtengo chili m'diso mwako? 4 Kodi unganene bwanji
kwa m'bale wako kuti, 'Ndikuchotse kachitsotso m'diso mwako,' pamene
nthawi zonse chimtengo uli nacho m'diso mwako? 5 Wachiphamaso iwe!
Yamba wachotsa chimtengo chili m'diso mwako ndipo pamenepo udzatha
kuona bwino ndi kuchotsa kachitsotso kali m'diso mwa m'bale wako.

6 "Musapatse agalu zinthu zopatulika; kapena musaponyere nkhumba
ngale zanu. Pakuti ngati mutero, zidzaziponda ndipo pomwepo zidza-
kutembenukirani ndi kukudulani nthulinthuli.

### *Pemphani, Funafunani, Gogodani*

7 “Pemphani ndipo mudzapatsidwa; funafunani ndipo mudzapeza;
gogodani ndipo adzakutsekulirani. 8 Pakuti wopempha aliyense ama-
landira; ndi wofuna amapeza; ndipo iye amene agogoda, adzamutsekulira.

9 “Ndani mwa inu, mwana wake akamupempha buledi amamupatsa
mwala? 10 Kapena ngati mwana apempha nsomba, kodi amamupatsa
njoka? 11 Tsono ngati inu woyipitsitsa mumadziwa kupatsa ana anu
mphatso zabwino, nanga Atate anu akumwamba sadzapereka mphatso
zabwino kwa iwo amene amupempha? 12 N’chifukwa chake zinthu
zilizonse mukafuna kuti anthu akuchitireni, yambani ndinu kuwachitira,
pakuti izi ndi zimene malamulo ndi aneneri amaphunzitsa.

### *Zipata Ziwiri ndi Njira Ziwiri*

13 “Lowani pa chipata chopapatiza. Pakuti chipata cholowera kuchi-
wonongeko n’chachikulu ndipo msewu wake ndi waukulunso. Ndipo
anthu ambiri amalowera pamenepo. 14 Koma chipata ndi chopapatiza ndi
msewu ndi waung’ono umene utsogolera anthu ku moyo wosatha ndipo
ndi owerengeka okha amene ayipeza njirayo.

### *Aneneri Owona ndi Onyenga*

15 “Chenjerani nawo aneneri onyenga. Amabwera kwa inu
atavala zikopa zankhosa, koma m’kati mwawo ali mimbulu yolusa.
16 Mudzawazindikira iwo ndi zipatso zawo. Kodi anthu amathyola mpesa
pa mtengo wa minga, kapena nkhuyu pa nthula? 17 Chimodzimodzinso
mtengo wabwino umabala chipatso chabwino, koma mtengo woyipa
umabala chipatso choyipa. 18 Mtengo wabwino sungabale chipatso
choyipa, ndi mtengo woyipa sungabale chipatso chabwino. 19 Mtengo
uliwonse umene subala chipatso chabwino umadulidwa ndi kuponyedwa
pa moto. 20 Momwemonso, ndi zipatso zawo iwo mudzawazindikira.

### *Ophunzira Owona ndi Onyenga*

21 “Si munthu aliyense amene amanena kwa Ine, ‘Ambuye, Ambuye,’
adzalowe mu ufumu wakumwamba, koma ndi yekhayo amene amachita
chifuniro cha Atate anga amene ali kumwamba. 22 Ambiri adzati kwa
Ine pa tsikulo, ‘Ambuye, Ambuye, kodi sitinkanenera m’dzina lanu ndi
m’dzina lanunso tinkatulutsa ziwanda ndi kuchita zodabwitsa zambiri?’
23 Pamenepo ndidzawawuza momveka bwino kuti, ‘Sindinakudziweni inu.
Chokani kwa Ine, inu ochita zoyipa!’

### *Womanga Nyumba Wanzeru ndi Wopusa*

24 “N’chifukwa chake aliyense amene amva mawu anga ndi kuwachita
akufanana ndi munthu wanzeru amene anamanga nyumba yake pa
thanthwe. 25 Mvula inagwa, mitsinje inadzaza, ndi mphepo zinawomba
pa nyumbayo; koma sinagwe, chifukwa maziko ake anali pa thanthwe.
26 Koma aliyense amene amva mawu angawa ndi kusawachita ali ngati
munthu wopusa amene anamanga nyumba yake pa mchenga. 27 Mvula
inagwa, mitsinje inadzaza, ndi mphepo zinawomba pa nyumbayo, ndipo
inagwa ndipo kugwa kwake kunali kwakukulu.”

28 Yesu atamaliza kunena zonsezi, magulu a anthu anadabwa ndi
chiphunzitso chake, 29 chifukwa anaphunzitsa ngati amene anali ndi
ulamuliro osati ngati aphunzitsi amalamulo.

# 8

### *Yesu Achiritsa Wakhate*

1 Iye atatsika ku phiri kuja, anthu ambirimbiri anamutsata. 2 Ndipo
munthu wakhate anadza kwa Yesu namugwadira nati, “Ambuye, ngati
mufuna, mukhoza kundiyeretsa.”

3 Yesu anatambasula dzanja lake namukhudza munthuyo nati, “Ndiku-
funa, yeretsedwa!” Nthawi yomweyo anachiritsidwa khate lake. 4 Ndipo
Yesu anati kwa iye, “Taona, usawuze wina aliyense. Koma upite kwa
mkulu wa ansembe ukadzionetse wekha ndi kupereka mphatso imene
Mose analamulira, kuti ukhale umboni kwa iwo.”

### *Chikhulupiriro cha Kenturiyo*

5 Yesu atalowa m’Kaperenamu, Kenturiyo anabwera kwa Iye napempha
chithandizo, 6 nati, “Ambuye, wantchito wanga ali chigonere ku nyumba,
sakuthanso kuyenda, akumva kuwawa kwambiri.”

7 Ndipo Yesu anati kwa iye, “Ine ndibwera kudzamuchiritsa.”

8 Kenturiyo uja anayankha kuti, “Ambuye, ndine wosayenera kuti Inu
mukalowe m’nyumba mwanga. Koma mungonena mawu ndipo wantchito
wanga adzachiritsidwa. 9 Pakuti inenso ndili pansi pa ulamuliro ndipo
ndili ndi asilikali amene ndiwalamulira. Ndikalamulira mmodzi kuti,
‘Pita,’ amapita; ndi kwa wina kuti, ‘Bwera,’ amabwera. Ndikawuza
wantchito wanga kuti, ‘Chita ichi,’ iye amachita.”

10 Yesu atamva zimenezi, anadabwa ndipo anati kwa omutsatira,
“Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti sindinapeze wina aliyense mu Israeli
wachikhulupiriro chachikulu chotere. 11 Ndikuwuzani kuti ambiri adzab-
wera kuchokera kummawa ndi kumadzulo, nadzakhala nawo pa phwando
pamodzi ndi Abrahamu, Isake ndi Yakobo mu ufumu wakumwamba.
12 Koma eni ake ufumuwo adzaponyedwa ku mdima wakunja kumene
kudzakhala kulira ndi kukukuta mano.”

13 Pamenepo Yesu anati kwa Kenturiyo, “Pita! Zichitike monga momwe
wakhulupirira.” Ndipo wantchito wake anachira pa nthawi yomweyo.

### *Yesu Achiritsa Anthu Ambiri*

14 Ndipo Yesu atalowa m’nyumba ya Petro, anaona mpongozi wake wa
Petro ali gone akudwala malungo. 15 Ndipo Yesu anakhudza dzanja lake
ndipo pomwepo anachira nayamba kumutumikira.

16 Itafika nthawi yamadzulo, anthu anabweretsa kwa Iye anthu ambiri
ogwidwa ndi ziwanda ndipo anatulutsa ziwandazo ndi mawu okha,
nachiritsa odwala onse. 17 Uku kunali kukwaniritsa zimene ananena
mneneri Yesaya kuti,

“Iye anatenga zofowoka zathu,
nanyamula nthenda zathu.”

### *Za Kutsatira Yesu*

18 Yesu ataona gulu la anthu litamuzungulira, analamula kuti awolokere
kutsidya lina la nyanja. 19 Ndipo mphunzitsi wa malamulo anabwera kwa
Iye nati, “Aphunzitsi, ine ndidzakutsatani kulikonse kumene muzipita.”

20 Yesu anayankha kuti, “Nkhandwe zili ndi mapanga ndi mbalame
zamlengalenga zili ndi zisa, koma Mwana wa Munthu alibe malo ogona
ngakhale potsamira mutu wake.”

21 Wophunzira wina anati kwa Iye, “Ambuye, mundilole ndiyambe
ndakayika maliro a abambo anga.”

22 Koma Yesu anamuwuza kuti, “Nditsate Ine ndipo uwaleke akufa
ayikane akufa okhaokha.”

### *Yesu Aletsa Namondwe*

23 Iye atalowa m’bwato, ophunzira ake anamutsatira. 24 Ndipo taonani
mwadzidzidzi mphepo yayikulu yamkuntho inawomba pa nyanjapo,
kotero kuti bwatolo linayamba kumizidwa ndi mafunde. Koma Yesu
anali mtulo. 25 Ophunzira ake anapita namudzutsa nati, “Ambuye!
Tipulumutseni! Tikumira!”
26 Iye anawayankha kuti, “Inu achikhulupiriro chochepa, chifukwa
chiyani mukuchita mantha?” Ndipo anayimirira nadzudzula mphepoyo
ndi mafunde ndipo panali bata lalikulu.
27 Ndipo ophunzirawo anadabwa nafunsa kuti, “Ndi munthu wotani
uyu? Kuti ngakhale mphepo ndi mafunde zimvera Iye!”

### *Ogwidwa ndi Ziwanda a ku Gadara*

28 Ndipo atafika ku mbali ina ya dera la Gadara, anakumana ndi anthu
awiri ogwidwa ndi ziwanda akuchokera ku manda. Iwowa anali woopsa
kwambiri kotero kuti panalibe munthu akanatha kudzera njira imeneyo.
29 Ndipo iwo anafuwulira kwa Yesu nati, “Mukufuna chiyani kwa ife, Inu
Mwana wa Mulungu? Kodi mwabwera kuno kudzatizunza nthawi yake
isanafike?”
30 Ndipo patali pake panali gulu la nkhumba zimene zimadya. 31 Ndipo
ziwandazo zinamupempha Yesu kuti, “Ngati mutitulutsa ife mutitumize
mu nkhumba izo.”
32 Iye anati kwa ziwandazo, “Pitani!” Ndipo pamenepo zinatuluka ndi
kukalowa m’nkhumbazo ndipo nkhumba zonse zinathamangira m’nyanja
ndi kufera momwemo. 33 Koma amene amaziweta anathawa nalowa
m’mudzi nafotokoza zonse, kuphatikizapo zimene zinachitika ndi anthu
ogwidwa ndi ziwanda aja. 34 Ndipo anthu onse a m’mudziwo anatuluka
kukakumana ndi Yesu. Ndipo atamuona Iye, anamupempha kuti achoke
m’dera lawo.

## 9

### *Munthu Wakufa Ziwalo wa ku Kaperenawo*

1 Yesu analowa m’bwato nawoloka, ndipo anabwera ku mudzi wa
kwawo. 2 Amuna ena anabwera ndi munthu wakufa ziwalo kwa Iye
atamugoneka pa mphasa. Yesu ataona chikhulupiriro chawo anati
kwa wakufa ziwaloyo, “Limba mtima mwana wanga, machimo ako
akhululukidwa.”
3 Pamenepo aphunzitsi ena amalamulo anaganiza mu mtima mwawo
kuti, “Munthu uyu akuchitira Mulungu mwano.”
4 Ndipo podziwa maganizo awo Yesu anati, “Bwanji mukuganiza zoyipa
m’mitima mwanu? 5 Chapafupi ndi chiti kunena kuti, ‘Machimo ako
akhululukidwa’ kapena kunena kuti, ‘Imirira ndipo yenda?’ 6 Tsono kuti
mudziwe kuti Mwana wa Munthu ali ndi ulamuliro pa dziko wokhululuka
machimo, pamenepo anati kwa wakufa ziwaloyo, ‘Imirira, tenga mphasa
yako kazipita kwanu.’ ” 7 Ndipo munthuyo anayimirira napita kwawo.
8 Gulu la anthu litaona izi, linadzazidwa ndi mantha ndipo linalemekeza
Mulungu amene anapereka ulamuliro kwa anthu.

### *Kuyitanidwa kwa Mateyu*

9 Ndipo Yesu atachoka kumeneko, anaona munthu wina dzina lake
Mateyu, atakhala m'nyumba ya msonkho. Anati kwa iye, "Nditsate Ine."
Ndipo iye ananyamuka namutsata.

10 Ndipo pamene Iye ankadya m'nyumba, onani, amisonkho ndi
ochimwa ambiri anabwera nakhala pansi pamodzi ndi Yesu ndi ophunzira
ake. 11 Ndipo Afarisi poona izi, anati kwa ophunzira ake, "N'chifukwa
chiyani Aphunzitsi anu akudya pamodzi ndi amisonkho ndi ochimwa?"

12 Yesu atamva, anati, "Munthu wamoyo safuna sing'anga ayi, koma
wodwala. 13 Koma pitani kaphunzireni tanthauzo la mawu awa: 'Ndi-
mafuna chifundo osati nsembe ayi.' Pakuti sindinabwere kudzayitana
olungama koma ochimwa."

### *Za Kusala Kudya*

14 Ndipo ophunzira a Yohane anabwera namufunsa Iye kuti, "Bwanji ife
ndi Afarisi timasala kudya koma ophunzira anu sasala kudya?"

15 Yesu anayankha kuti, "Kodi oyitanidwa ku ukwati angamalire bwanji
pamene mkwati ali naye pamodzi? Nthawi idzafika pamene mkwatiyo
adzachotsedwa ndi pamene adzasala kudya."

16 Ndipo palibe munthu amasokerera chigamba chatsopano pa chovala
chakale chifukwa chigambacho chidzachoka ndipo chibowocho chidza-
kula kuposa kale. 17 Kapena sathira vinyo watsopano m'matumba
akale; akatero, matumba akalewo adzaphulika ndipo vinyoyo adzatayika,
matumbawo adzawonongeka; satero ayi. Amathira vinyo watsopano
m'matumba atsopanonso ndipo zonse zimasungika.

### *Za Mwana Wamkazi wa Yairo ndi Mayi Wokhudza Chovala cha Yesu*

18 Pamene ankanena zimenezi, mkulu wa sunagoge anabwera namug-
wadira Iye nati, "Mwana wanga wamkazi wamwalira posachedwapa
koma tiyeni mukasanjike dzanja lanu pa iye ndipo adzakhala ndi moyo."
19 Yesu ndi ophunzira ake ananyamuka napita naye pamodzi.

20 Panali mayi wina amene ankadwala nthenda yotaya magazi kwa zaka
khumi ndi ziwiri ndipo anadza m'mbuyo mwake nakhudza mkanjo wake.
21 Iyeyo anati mwa iye yekha, "Nditangokhudza kasonga ka mkanjo wake,
ine ndidzachiritsidwa."

22 Ndipo Yesu anatembenuka namuona mayiyo nati, "Limbani mtima
mayi iwe, chikhulupiriro chako chakuchiritsa." Nthawi yomweyo mayiyo
anachiritsidwa.

23 Yesu atalowa m'nyumba ya mkulu wa sunagoge ndi kuona oyimba
zitoliro ndi gulu la anthu ochita phokoso, 24 anati, "Tulukani, mtsikanayu
sanafe koma ali mtulo." Koma anamuseka Iye. 25 Atangowatulutsa
anthuwo, analowa m'nyumba ndipo anagwira dzanja la mtsikanayo ndipo
anauka. 26 Mbiriyi inamveka m'dera lonse.

### *Yesu Achiritsa Osaona ndi Osayankhula*

27 Yesu atapitirira ulendo wake, amuna awiri osaona anamutsatira Iye,
akufuwula kuti, "Tichitireni chifundo, Mwana wa Davide!"

28 Atalowa m'nyumba, amuna awiri osaonawo anabwera kwa Iye ndipo
anawafunsa kuti, "Kodi mukhulupirira kuti ndikhoza kukuchiritsani?"

Iwo anayankha kuti, "Inde Ambuye."

29 Pomwepo anakhudza maso awo nati, “Zichitike kwa inu monga
mwachikhulupiriro chanu.” 30 Ndipo anayamba kuona. Yesu anawachen-
jeza kwambiri nati, “Onani, wina aliyense asadziwe za zimenezi.” 31 Koma
iwo anatuluka m’nyumbamo nafalitsa za Iye m’chigawo chonse.
32 Pamene iwo ankatuluka kunja, anthu anabwera kwa Iye ndi munthu
wogwidwa ndi mzimu wosayankhula. 33 Ndipo atatulutsa mzimuwo,
munthuyo anayankhula. Gulu la anthuwo linadabwa ndipo linati, “Zinthu
zotere sizinaonekepo mu Israeli.”
34 Koma Afarisi anati, “Akutulutsa mizimu yoyipa ndi mphamvu ya
mkulu wa ziwanda.”

### *Antchito ndi Ochepa*

35 Yesu anayendayenda m’mizinda yonse ndi m’midzi, kuphunzitsa
m’masunagoge awo, nalalikira Uthenga Wabwino wa ufumu ndi kuchir-
itsa nthenda zawo zonse ndi zofowoka za m’matupi mwawo. 36 Ataona
maguluwo, anagwidwa ndi chisoni chifukwa anali ozunzika ndi osowa
chithandizo ngati nkhosa zopanda m’busa. 37 Pamenepo anati kwa ophun-
zira ake, “Zokolola ndi zambiri koma antchito ndi ochepa. 38 N’chifukwa
chake, pemphani Ambuye mwini zokolola kuti atumize antchito ku munda
wake.”

## 10

### *Yesu Atuma Ophunzira Ake*

1 Yesu anayitana ophunzira ake khumi ndi awiri ndipo anawapatsa
ulamuliro otulutsa mizimu yoyipa ndi kuchiritsa nthenda iliyonse ndi
zofowoka zilizonse.
2 Mayina a atumwi khumi ndi awiriwo ndi awa: woyamba, Simoni
(wotchedwa Petro) ndi m’bale wake Andreya; Yakobo mwana wa Zebe-
dayo ndi m’bale wake Yohane, 3 Filipo ndi Bartumeyu, Tomasi ndi Mateyu
wolandira msonkho, Yakobo mwana wa Alufeyo ndi Tadeyo; 4 Simoni
Mzerote ndi Yudasi Isikarioti, amene anamupereka Iye.
5 Yesu anatuma khumi ndi awiriwo ndi kuwalamula kuti, “Musapite
kwa anthu a mitundu ina kapena kulowa m’mudzi uliwonse wa
Asamariya. 6 Koma pitani kwa nkhosa zotayika za banja la Israeli.
7 Pamene mukupita, muzikalalikira uthenga uwu: ‘Ufumu wakumwamba
wayandikira.’ 8 Chiritsani odwala, ukitsani akufa, chiritsani akhate,
tulutsani ziwanda. Munalandira kwaulere, perekani kwaulere.
9 “Musatenge ndalama zagolide kapena zasiliva kapena zakopala
m’zikwama mwanu; 10 musatenge thumba la paulendo, kapena malaya
awiri kapena nsapato kapena ndodo; pakuti wantchito ayenera kulandira
chakudya chake. 11 Mukalowa mu mzinda ndi m’mudzi uliwonse,
funafunani munthu woyenera ndipo mukhale m’nyumba mwake kufikira
mutachoka. 12 Pamene mulowa m’nyumba mupereke moni. 13 Mtendere
wanu ukhale pa a m’nyumbayo ngati ndi oyenera. Koma ngati siwoyenera,
mtendere wanu ubwerere kwa inu. 14 Ngati wina aliyense sakakulandi-
rani kapena sakamvera mawu anu, musase fumbi la kumapazi anu
pamene mutuluka m’nyumbayo kapena mu mzindawo. 15 Zoonadi, Ine
ndikuwuzani kuti pa tsiku lachiweruziro, mlandu wa Sodomu ndi Gomora
udzachepa kusiyana ndi wa mzindawo.
16 “Taonani ndikukutumizani inu monga nkhosa pakati pa mimbulu.
Chifukwa chake khalani ochenjera ngati njoka ndi woona mtima ngati

nkhunda. [17] Chenjerani ndi anthu pakuti adzakuperekani ku mabwalo
amilandu nadzakukwapulani m'masunagoge mwawo. [18] Chifukwa cha
Ine, mudzaperekedwa kwa olamulira ndi kwa mafumu kuti mukhale
mboni kwa iwo ndi kwa a mitundu ina. [19] Koma pamene akumangani,
inu musadandaule kuti mukanena bwanji kapena mukanena chiyani.
Mudzapatsidwa pa nthawi imeneyo zoti munene, [20] pakuti sindinu
mudzanena, koma Mzimu Woyera wa Atate anu, adzayankhula mwa inu.

[21] "M'bale adzapereka m'bale kuti aphedwe ndi abambo mwana wawo:
ndipo ana adzawukira makolo awo ndi kuwapereka kuti aphedwe.
[22] Anthu onse adzada inu chifukwa cha Ine, koma iye amene apirira mpaka
kumapeto, adzapulumuka. [23] Pamene akuzunzani pamalo ena thawirani
kwina. Pakuti ndikuwuzani zoonadi kuti simudzamaliza mizinda yonse
ya Israeli Mwana wa Munthu asanabwere.

[24] "Wophunzira saposa mphunzitsi wake ndipo wantchito saposa bwana
wake. [25] N'koyenera kuti wophunzira akhale ngati mphunzitsi wake,
ndi wantchito akhale ngati bwana wake. Ngati mwini banja atchedwa
Belezebabu, koposa kotani a m'nyumba mwake!

[26] "Chifukwa chake musaope iwo. Pakuti palibe chinthu chobisika
chimene sichidzavundukulidwa, ndi chobisika chimene sichidzadziwika.
[27] Chimene ndikuwuzani Ine mu mdima, muchiyankhule poyera; chimene
akunong'onezani m'khutu, muchilalikire muli pa denga. [28] Musamaope
amene amapha thupi koma sangathe kuchotsa moyo. Koma muziopa Iye
amene akhoza kupha mzimu ndi kuwononga thupi mu gehena. [29] Kodi
suja amagulitsa mbalame ziwiri ndi ndalama imodzi? Koma palibe
imodzi ya izo imene idzagwa pansi wopanda chifuniro cha Atate anu.
[30] Ndipo ngakhale tsitsi la m'mutu mwanu linawerengedwa kale. [31] Potero
musaope; inu ndinu a mtengo woposa mbalame zambiri.

[32] "Aliyense amene avomereza Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidza-
vomereza pamaso pa Atate anga akumwamba. [33] Koma iye amene
andikana Ine pamaso pa anthu, Inenso ndidzamukana pamaso pa Atate
anga akumwamba.

[34] "Musaganize kuti Ine ndabweretsa mtendere pa dziko lapansi. Sind-
inabwere kudzapereka mtendere koma lupanga. [35] Pakuti Ine ndabwera
kudzalekanitsa

" 'Munthu ndi abambo ake,
mwana wamkazi ndi amayi ake,
mtengwa kulekanitsidwa ndi apongozi ake,
[36] adani a munthu adzakhala a m'banja mwake momwe.'

[37] "Aliyense amene akonda abambo kapena amayi ake koposa Ine
sayenera kukhala wanga; aliyense amene akonda mwana wake wamwa-
muna kapena wamkazi koposa Ine sayenera kukhala wanga. [38] Aliyense
amene satenga mtanda wake ndi kunditsata Ine sayenera kukhala wanga.
[39] Aliyense amene asunga moyo wake adzawutaya koma aliyense amene
ataya moyo chifukwa cha Ine adzawupeza.

[40] "Iye amene alandira inu alandira Ine, ndipo amene alandira
Ine alandiranso amene ananditumа Ine. [41] Aliyense amene alandira
mneneri chifukwa chakuti ndi mneneri alandira mphotho ya mneneri,
ndipo aliyense amene alandira munthu wolungama chifukwa chakuti
ndi munthu wolungama, adzalandira mphotho ya wolungama.
[42] Ngati aliyense apereka madzi ozizira a m'chikho kwa mmodzi wa

ang'onoang'ono awa chifukwa cha kuti ndi ophunzira anga, ndikuwuzani
zoona, ndithudi sadzataya mphotho yake."

# 11

### *Otumidwa ndi Yohane M'batizi*

1 Ndipo Yesu atamaliza kulangiza ophunzira ake khumi ndi awiri aja,
anachoka kumeneko kupita kukaphunzitsa ndi kukalalikira ku mizinda
ya ku Galileya.
2 Yohane ali m'ndende anamva zimene Khristu ankachita, ndipo
anatumiza ophunzira ake kukamufunsa Iye. 3 Anamufunsa kuti, "Kodi
Inu ndinu uja ankanena kuti mudzabwerayu kapena tidikire wina?"
4 Yesu anayankha kuti, "Bwererani ndi kukamuwuza Yohane zimene
mwamva ndi kuona. 5 Osaona akuona, olumala akuyenda, akhate akuchir-
itsidwa, osamva akumva, akufa akuukitsidwa ndipo Uthenga Wabwino
ukulalikidwa kwa osauka. 6 Odala ndi munthu amene sakhumudwa
chifukwa cha Ine."
7 Pamene ophunzira a Yohane ankachoka, Yesu anayamba kuyankhula
kwa gulu la anthu za Yohane kuti, "Kodi munkapita ku chipululu kuti
mukaone chiyani? Kodi bango logwedezeka ndi mphepo? 8 Nanga
munkapita kukaona chiyani, munthu wovala zokongola? Ayi, wovala
zokongola amakhala m'nyumba za mafumu. 9 Nanga munkapita kukaona
chiyani? Mneneri kodi? Inde ndikuwuzani kuti munkakaona woposa
mneneri. 10 Uyu ndi amene malemba akunena za iye kuti,
"Ine ndidzatuma mthenga wanga patsogolo panu
amene adzakonza njira yanu.
11 Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti pakati pa obadwa ndi mkazi sipanaoneke
wina aliyense wamkulu woposa Yohane M'batizi; komatu amene ndi
wamng'ono kwambiri mu ufumu wakumwamba ndi wamkulu koposa
iye. 12 Kuyambira masiku a Yohane M'batizi mpaka tsopano, ufumu
wakumwamba ndi wolimbirana ndipo anthu amphamvu okha ndi amene
akuwulanda. 13 Pakuti aneneri onse ndi malamulo ananenera kufikira
nthawi ya Yohane. 14 Ndipo ngati inu mufuna kulandira izi, iyeyu ndi
Eliya amene ankanena kuti adzabwera uja. 15 Iye amene ali ndi makutu
amve.
16 "Kodi m'bado uwu ndingawufanizire ndi chiyani? Uli ngati ana
opezeka m'misika amene akuyitana anzawo n'kumati:
17 " 'Tinakuyimbirani zitoliro,
koma inu simunavine;
ife tinayimba nyimbo zamaliro,
koma inu simunalire.'
18 Pakuti Yohane sanabwerere kudya kapena kumwa koma iwo ankanena
kuti, 'Iye anali ndi chiwanda.' 19 Mwana wa Munthu anabwera ndi
kumadya ndi kumwa koma iwo akuti, 'Munthu wadyera, woledzera,
bwenzi la amisonkho ndi bwenzi la ochimwa.' Koma nzeru imatsimikizika
kuti ndi yolondola mwa ntchito zake."

### *Tsoka la Mizinda Itatu Yosatembenuka mtima*

20 Pamenepo Yesu anayamba kudzudzula mizinda imene zodabwitsa
zake zambiri zinachitikamo, chifukwa chakuti sinatembenuke mtima.
21 "Tsoka kwa iwe Korazini! Tsoka kwa iwe Betisaida! Ngati zodab-
witsa zimene zinachitika mwa iwe zikanachitidwa mu Turo ndi Sidoni,
iwo akanalapa kale atavala ziguduli ndi kudzola phulusa. 22 Koma

ndikuwuzani inu kuti pa tsiku lachiweruzo mlandu wa Turo ndi Sidoni
udzachepako kusiyana ndi wanu. [23] Ndipo iwe Kaperenawo, kodi udzak-
wezedwa kufika kumwamba? Ayi, udzatsitsidwa mpaka pansi kufika ku
Hade. Ngati zodabwitsa zimene zinachitika mwa iwe, zikanachitika mu
Sodomu, bwenzi iye alipo kufikira lero. [24] Koma Ine ndikuwuzani kuti
pa tsiku la chiweruziro mlandu wa Sodomu udzachepako kusiyana ndi
wanu."

### *Goli la Khristu*

[25] Pa nthawi imeneyo Yesu anati, "Ine ndikukuyamikani Inu Atate
Ambuye akumwamba ndi dziko lapansi, chifukwa Inu mwawabisira
zinthu izi anzeru ndi ophunzira ndi kuziwulula kwa ana ang'onoang'ono.
[26] Inde, Atate, ichi chinali chokukomerani Inu.
[27] "Zinthu zonse zapatsidwa kwa Ine ndi Atate anga. Palibe mmodzi
amene adziwa Mwana kupatula Atate ndipo palibe mmodzi amene
adziwa Atate kupatula Mwana ndi kwa iwo amene Mwana awasankha
kuwawululira.
[28] "Idzani kwa Ine, inu nonse otopa ndi olemedwa ndipo Ine ndidzaku-
patsani mpumulo. [29] Senzani goli langa ndipo phunzirani kwa Ine, pakuti
ndine wofatsa ndi wodzichepetsa. Ndipo inu mudzapeza mpumulo wa
miyoyo yanu. [30] Pakuti goli langa ndi losavuta ndipo katundu wanga ndi
wopepuka."

## 12

### *Yesu Mbuye wa Sabata*

[1] Pa nthawi imeneyo Yesu anadutsa pakati pa minda ya tirigu pa tsiku
la Sabata. Ophunzira ake anamva njala nayamba kuthyola ngala za tirigu
n'kumadya. [2] Afarisi ataona zimenezi anati kwa Iye, "Taonani! Ophunzira
anu akuchita zosaloledwa pa tsiku la Sabata."
[3] Iye anayankha kuti, "Kodi simunawerenge zimene anachita Davide
pamene iye ndi anzake anamva njala? [4] Analowa m'Nyumba ya Mulungu,
ndipo iye ndi anzakewo anadya buledi wopatulika amene sikunali
kololedwa kwa iwo kudya koma ansembe okha. [5] Kodi simunawerenge
m'malamulo kuti pa Sabata ansembe m'Nyumba ya Mulungu amaph-
wanya lamulo la Sabata komabe sawayesa olakwa? [6] Ine ndikuwuzani kuti
wamkulu kuposa Nyumba ya Mulunguyo ali pano. [7] Ngati mukanadziwa
zomwe mawu awa atanthauza, 'Ine ndifuna chifundo osati nsembe,' inu
simukanatsutsa osalakwa. [8] Pakuti Mwana wa Munthu ndiye Mbuye wa
Sabata."

### *Yesu Achiritsa Munthu Wolumala Dzanja*

[9] Atachoka kumeneko anakalowa m'sunagoge mwawo. [10] Ndipo
m'menemo munali munthu wolumala dzanja. Pofuna chifukwa choka-
munenezera, iwo anamufunsa Yesu kuti, "Kodi n'kololedwa kuchiritsa
munthu tsiku la Sabata?"
[11] Iye anawawuza kuti, "Ngati wina wa inu ali ndi nkhosa nig-
wera m'dzenje tsiku la Sabata, kodi simudzayigwira ndi kuyitulutsa
kunja? [12] Nanga munthu sali oposa nkhosa kwambiri! Chifukwa chake
n'kololedwa kuchita zabwino pa Sabata."
[13] Pamenepo Yesu anati kwa munthuyo, "Wongola dzanja lako." Iye
analiwongola ndipo linakhala monga linalili kale. [14] Koma Afarisi
anatuluka kunja ndi kukonza njira yoti amuphere.

### *Mtumiki Wosankhidwa ndi Mulungu*

15 Podziwa zimenezi, Yesu anachoka kumalo amenewo. Ambiri
anamutsata Iye ndipo anachiritsira odwala awo onse 16 nawachenjeza
kuti asamuwulule kuti yani. 17 Uku kunali kukwaniritsa zimene zi-
nayankhulidwa kudzera mwa mneneri Yesaya kuti,

18 “Taonani mnyamata wanga amene ndinamusankha,
Wokondedwa wanga, amene moyo wanga ukondwera naye.
Pa Iye ndidzayika Mzimu wanga,
ndipo Iye adzalalikira chiweruzo kwa akunja.
19 Sadzalimbana, sadzafuwula,
ngakhale mmodzi sadzamva mawu ake m’makwalala.
20 Bango lophwanyika sadzalithyola,
ndi nyale yofuka sadzayizimitsa,
kufikira Iye adzatumiza chiweruziro chikagonjetse.
21 Ndipo akunja adzakhulupirira dzina lake.”

### *Mwano wa Afarisi*

22 Pomwepo anthu anabwera naye kwa Yesu munthu wogwidwa ndi
chiwanda amene anali wosaona ndi wosamva ndipo Yesu anamuchiritsa
kotero kuti atatha anayamba kumva ndi kuona. 23 Anthu onse anadabwa
ndipo anati, “Kodi uyu ndi kukhala mwana wa Davide?”
24 Koma Afarisi atamva zimenezi, anati, “Uyu amatulutsa ziwanda ndi
mphamvu ya Belezebabu mkulu wa ziwandazo.”
25 Yesu anadziwa maganizo awo ndipo anawawuza kuti, “Ufumu
uliwonse ukagawanika mwa iwo udzawonongeka ndi mzinda uliwonse
kapena banja likagawanika, mwa izo zokha sizidzayima. 26 Ngati Satana
atulutsa Satana, iye adzigawa yekha. Nanga ufumu wake ungayime
bwanji? 27 Ndipo ngati Ine nditulutsa ziwanda ndi Belezebule, anthu
anu amatulutsa ziwandazo ndi chiyani? Potero tsono adzakhala oweruza
anu. 28 Koma ngati Ine ndimatulutsa ziwanda ndi Mzimu wa Mulungu,
pamenepo ufumu wa Mulungu wafika pa inu.
29 “Kapenanso wina aliyense angathe bwanji kulowa m’nyumba ya
munthu wamphamvu ndi kunyamulamo zinthu zake, sipokhapo atayamba
wamanga munthu wa mphamvuyo? Pamenepo iye akhoza kuba
m’nyumbamo.
30 “Iye amene sali ndi Ine atsutsana nane ndipo iye amene sasonkhanitsa
pamodzi ndi Ine amamwaza. 31 Ndipo potero Ine ndikuwuzani inu, tchimo
lililonse ndi cha mwano chilichonse zidzakhululukidwa kwa anthu koma
chamwano cha pa Mzimu Woyera, sichidzakhululukidwa. 32 Aliyense
amene anena mawu otsutsana ndi Mwana wa Munthu adzakhululukidwa
koma aliyense wonena motsutsana ndi Mzimu Woyera sadzakhululukidwa
mu m’bado uno kapena umene ukubwerawo.

### *Mtengo ndi Zipatso Zake*

33 “Mtengo wabwino umabala zipatso zabwino ndipo mtengo woyipa
umabalanso zipatso zoyipa, pajatu mtengo umadziwika ndi zipatso zake.
34 Ana anjoka inu, woyipa inu, mungathe bwanji kuyankhula kanthu
kalikonse kabwino? Pakuti pakamwa pamayankhula zosefuka kuchokera
mu mtima. 35 Munthu wabwino amatulutsa zinthu zabwino zomwe zili
mumtima mwake ndipo munthu woyipa amatulutsanso zinthu zoyipa
zomwe zili mwa iye. 36 Ine ndikukuwuzani kuti pa tsiku la chiweruziro
munthu adzazengedwa mlandu chifukwa cha mawu aliwonse wopanda

pake amene anayankhula. 37 Pakuti ndi mawu anu mudzapezeka
osalakwa ndiponso ndi mawu anu mudzapezeka olakwa.”

*Chizindikiro cha Yona*

38 Pamenepo ena mwa Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo anati kwa Iye,
“Aphunzitsi, tikufuna tione chizindikiro chodabwitsa kuchokera kwa Inu.”
39 Iye anayankha kuti, “M’bado woyipa ndi wachigololo ufunsa za
chizindikiro chodabwitsa! Koma ndi chimodzi chomwe sichidzapatsidwa
kwa inu kupatula chizindikiro cha mneneri Yona. 40 Pakuti monga Yona
anali m’mimba mwa nsomba yayikulu masiku atatu, usana ndi usiku,
momwemonso Mwana wa Munthu adzakhala masiku atatu, usana ndi
usiku, m’kati mwa nthaka. 41 Anthu a ku Ninive adzayimirira pachiweruzo
ndi m’bado uwu ndi kuwutsutsa pakuti iwo analapa Yona atalalikira
ndipo tsopano wamkulu kuposa Yona ali pano. 42 Mfumu yayikazi
yakummwera idzayimirira pa tsiku lachiweruzo ndi m’bado uwu ndipo
idzawutsutsa pakuti inachokera kumathero a dziko lapansi kudzamva
nzeru za Solomoni, ndipo pano pali woposa Solomoni.

*Za Mzimu Woyipa*

43 “Pamene mzimu woyipa utuluka mwa munthu, umadutsa
malo wopanda madzi kufunafuna malo opumulira ndipo suwapeza.
44 Pamenepo umati, ‘Ndidzabwerera ku nyumba yanga komwe
ndinatuluka.’ Pamene ufika, upeza mopanda kanthu, mosesedwa ndi
mokonzedwa bwino. 45 Kenaka umapita kukatenga mizimu ina isanu
ndi iwiri yoyipa kwambiri kuposa uwowo ndipo imapita ndi kukakhala
m’menemo. Choncho khalidwe lotsiriza la munthu uyu limakhala loyipa
kwambiri kuposa loyambalo. Umo ndi mmene zidzakhalire ndi m’bado
oyipawu.”

*Amayi ndi Abale Ake a Yesu*

46 Pamene Yesu anali kuyankhulabe ndi gulu la anthu, amayi ndi abale
ake anayimirira kunja, akufuna kuyankhulana naye. 47 Wina anamuwuza
Iye kuti, “Amayi ndi abale anu ayima kunjaku akufuna kuyankhulana
nanu.”
48 Iye anayankha kuti, “Amayi anga ndani ndipo abale anga ndi ndani?”
49 Ndipo akuloza ophunzira ake, Iye anati, “Awa ndiwo amayi anga ndi
abale anga. 50 Pakuti aliyense amene achita chifuniro cha Atate anga
akumwamba ndiye m’bale wanga, mlongo wanga ndi amayi anga.”

# 13

*Fanizo la Wofesa Mbewu*

1 Tsiku lomwelo Yesu anatuluka m’nyumba ndipo anakhala m’mbali
mwa nyanja. 2 Magulu a anthu anasonkhana mozungulira ndipo Iye
analowa m’bwato nakhala pansi ndipo anthu onse anayimirira ku
mtunda. 3 Pamenepo Iye anawawuza zinthu zambiri m’mafanizo ndi kuti,
“Mlimi anapita kukafesa mbewu zake. 4 Akufesa, zina zinagwera m’mbali
mwa njira ndipo mbalame zinabwera ndi kuzidya. 5 Zina zinagwa pamalo
a miyala pamene panalibe dothi lambiri. Zinamera mofulumira chifukwa
panalibe dothi lambiri. 6 Koma dzuwa litakwera, mbewu zinapserera
ndipo zinawuma chifukwa zinalibe mizu. 7 Mbewu zina zinagwa pa minga
ndipo mingayo inayanga ndi kuzirepheretsa kukula. 8 Koma mbewu zina
zinagwa pa nthaka yabwino ndipo zinabala zipatso 100, zina 60 ndipo

zinanso makumi atatu mwa zimene zinafesedwa. 9 Amene ali ndi makutu
amve.”
10 Ophunzira anabwera kwa Iye ndikumufunsa kuti, “Chifukwa chiyani
Inu mukuyankhula kwa anthu m’mafanizo?”
11 Iye anayankha kuti, “Nzeru zakudziwa zinsinsi za ufumu
wakumwamba zapatsidwa kwa inu koma osati kwa iwo. 12 Aliyense
amene ali nazo adzapatsidwa zowonjezera ndipo iye adzakhala nazo
zambiri. Aliyense amene alibe, ngakhale zimene ali nazo adzamulanda.
13 Ichi ndi chifukwa chake ndimayankhula kwa iwo m’mafanizo:
“Ngakhale akupenya koma saona,
ngakhale akumva koma samvetsetsa kapena kuzindikira.
14 Mwa iwo zimene ananenera Yesaya zikwaniritsidwa:
“ ‘Kumva mudzamva koma osamvetsetsa.
Kupenya mudzapenya koma osaona kanthu.
15 Pakuti mtima wa anthu awa ndi wokanika,
m’makutu mwawo ndi mogontha,
ndipo atsinzina
kuti asaone kanthu.
Mwina angapenye ndi maso awo,
angamve ndi makutu awo, angamvetse ndi nzeru zawo ndi kutembe-
nuka,
Ineyo n’kuwachiritsa.’
16 Koma maso anu ndi odala chifukwa amapenya ndi makutu anu
chifukwa amamva. 17 Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti aneneri ambiri ndi
anthu olungama anafuna kuona zimene inu mukupenya koma sanazione
ndi kumva zimene inu mukumva koma sanazimve.

### *Tanthauzo la Fanizo la Wofesa*

18 “Tamverani tsono zimene fanizo la wofesa litanthauza: 19 Pamene
aliyense akumva uthenga wa ufumu koma sawuzindikira, woyipayo
amabwera ndi kuchotsa zimene zafesedwa mu mtima mwake. Iyi ndi
mbewu yofesedwa m’mbali mwa njira. 20 Zimene zinafesedwa pa malo
amiyala ndi munthu amene amamva mawu ndi kuwalandira msanga
ndi chimwemwe. 21 Koma popeza alibe muzu, iwo amakhala nthawi
yochepa. Pamene vuto kapena zunzo libwera chifukwa cha mawu, iye
amagwa mofulumira. 22 Zimene zinafesedwa pakati pa minga, ndi munthu
amene amamva mawu koma nkhawa za moyo uno ndi chinyengo cha
chuma zimalepheretsa mawuwo kuti abale chipatso. 23 Koma zimene
zinafesedwa pa nthaka yabwino, ndi munthu amene amamva mawu
ndipo amawazindikira. Iye amabala zipatso zokwanira 100, zina 60 ndipo
zinanso makumi atatu mwa zimene zinafesedwa.”

### *Fanizo la Namsongole*

24 Yesu anawawuza fanizo lina kuti: “Ufumu wakumwamba ufanana
ndi munthu amene anafesa mbewu zabwino m’munda mwake. 25 Koma
aliyense akugona usiku mdani wake anabwera ndi kufesa namsongole
pakati pa tirigu ndipo anachoka. 26 Pamene tirigu anamera ndi kutulutsa
ngala, namsongole anaonekanso.
27 “Antchito ake anabwera kwa iye ndi kuti, ‘Bwana, kodi simunafese
mbewu zabwino m’munda mwanu? Nanga namsongole wachokera kuti?’
28 “Iye anayankha kuti, ‘Ndi mdani amene anachita izi.’
“Antchito anamufunsa iye kuti, ‘Kodi mufuna kuti tipite tikamuzule?’

29 “Iye anakana nati, ‘Ayi. Chifukwa pamene mukuzula namsongoleyo
mwina inu mungazulire pamodzi ndi tirigu. 30 Zisiyeni zonse zikulire
pamodzi mpaka nthawi yokolola. Pa nthawi imeneyo ndidzawuza okolola
kuti: Poyamba sonkhanitsani namsongole ndi kumumanga m’mitolo
kuti atenthedwe, kenaka sonkhanitsani tirigu ndi kumuyika m’nkhokwe
yanga.’ ”

### *Fanizo la Mbewu ya Mpiru ndi Yisiti*

31 Iye anawawuza fanizo lina kuti, “Ufumu wakumwamba uli ngati
mbewu ya mpiru, imene munthu anatenga ndi kudzala m’munda
mwake. 32 Ngakhale mbewuyi ndi yaying’ono mwa mbewu zanu
zonse za m’munda, imakula ndi kukhala mtengo kotero kuti mbalame
zamlengalenga zimabwera ndi kupumula m’nthambi zake.”
33 Iye anawawuzanso fanizo lina nati: “Ufumu wakumwamba ufanana
ndi yisiti amene mayi anatenga ndi kusakaniza mu ufa wambiri mpaka
wonse unafufuma.”
34 Yesu anayankhula zinthu zonsezi kwa gulu la anthu m’mafanizo ndipo
Iye sananene kalikonse kwa iwo osagwiritsa ntchito fanizo. 35 Kotero
zinakwaniritsidwa zimene zinayankhulidwa ndi mneneri kuti,
“Ndidzatsekula pakamwa panga ndi mafanizo,
ndidzawulula zinthu zobisika
chiyambire kukhazikidwa kwa dziko lapansi.”

### *Yesu Awatanthauzira Fanizo la Namsongole*

36 Kenaka Iye anasiya gulu la anthu ndi kukalowa m’nyumba. Ophun-
zira ake anapita kwa Iye nati, “Timasulireni fanizo la namsongole
m’munda.”
37 Iye anayankha nati, “Munthu amene anafesa mbewu yabwino ndi
Mwana wa Munthu. 38 Munda ndi dziko lapansi ndipo mbewu yabwino
ndi ana a ufumu. Namsongole ndi ana a woyipayo. 39 Ndipo amene
anafesa namsongole ndi Satana. Kukolola ndiko kutha kwa dzikoli ndipo
otuta ndi angelo.
40 “Monga momwe namsongole azulidwa ndi kutenthedwa ndi moto,
momwemonso kudzakhala pakutha kwa dziko. 41 Mwana wa Munthu
adzatumiza angelo ake ndipo iwo adzachotsa mu ufumu wake chili-
chonse chochimwitsa ndi onse amene amachita zoyipa. 42 Adzawaponya
m’ng’anjo yamoto kumene kudzakhala kulira ndi kukuta mano.
43 Pamenepo olungama adzawala ngati dzuwa mu ufumu wa Atate awo.
Amene ali ndi makutu amve.”

### *Fanizo la Chuma Chobisika ndi la Ngale*

44 “Ufumu wakumwamba ufanana ndi chuma chobisika m’munda.
Munthu atachipeza anachibisanso ndipo ndi chimwemwe anapita nakag-
ulitsa zonse anali nazo, nakagula mundawo.
45 “Komanso Ufumu wakumwamba ufanana ndi wogulitsa malonda
amene amafuna ngale zabwino. 46 Atapeza imodzi ya mtengowapatali,
iye anapita nakagulitsa chilichonse anali nacho ndi kukayigula.”

### *Fanizo la Khoka*

47 “Komanso Ufumu wakumwamba ufanana ndi khoka limene
linaponyedwa m’nyanja ndipo linakola mitundu yonse ya nsomba.
48 Litadzaza, asodzi analikokera ku mtunda. Pomwepo anakhala pansi
nasonkhanitsa nsomba zabwino m’madengu koma zoyipa anazitaya.

49 Umu ndi mmene kudzakhalira pakutha kwa dziko. Angelo adzabwera
ndi kulekanitsa oyipa ndi olungama. 50 Ndipo oyipa adzawaponya
m'ng'anjo ya moto kumene kudzakhala kulira ndi kukukuta mano."

51 Yesu anawafunsa kuti, "Kodi mwamvetsetsa zonsezi?"

Iwo anayankha kuti, "Inde."

52 Iye anawawuza kuti, "Chifukwa chake mphunzitsi aliyense wa
malamulo amene walangizidwa za ufumu wakumwamba ali ngati mwini
nyumba amene amatulutsa chuma chatsopano komanso chakale."

### *Amupeputsa Yesu ku Nazareti*

53 Yesu atatsiriza mafanizowa anachoka kumeneko. 54 Atafika ku mudzi
kwawo anayamba kuphunzitsa m'masunagoge awo ndipo iwo anadabwa
nati, "Munthu uyu anayitenga kuti nzeru iyi ndi mphamvu zodabwitsazi?
55 Kodi si mwana wa wopala matabwa? Kodi dzina la amayi ake si Mariya
ndipo kodi abale ake si Yakobo, Yosefe, Simoni ndi Yudasi? 56 Kodi alongo
ake onse sali ndi ife? Tsono ndi kuti kumene anazitenga zinthu izi?"
57 Ndipo iwo anakhumudwa chifukwa cha Iye.

Koma Yesu anawawuza kuti, "Mneneri sapatsidwa ulemu ku mudzi
kwawo ndi ku nyumba kwawo."

58 Ndipo Iye sanachite zodabwitsa zambiri kumeneko chifukwa cha
kusowa kwa chikhulupiriro kwawo.

## 14

### *Kuphedwa kwa Yohane M'batizi*

1 Pa nthawi imeneyo Mfumu Herode anamva za mbiri ya Yesu. 2 Ndipo
iye anati kwa antchito ake, "Uyu ndi Yohane M'batizi; iye wauka kwa
akufa! Ichi ndi chifukwa chake mphamvu zodabwitsa zikugwira ntchito
mwa iye."

3 Pakuti Herode anamugwira Yohane ndi kumumanga ndipo anamuyika
m'ndende chifukwa cha Herodia mkazi wa m'bale wake Filipo. 4 Chifukwa
Yohane anakhala akunena kwa iye kuti, "Sichololedwa kwa inu kutenga
mkaziyo." 5 Herode anafuna kupha Yohane koma iye anaopa anthu
chifukwa anamuyesa iye mneneri.

6 Pa tsiku lokumbukira kubadwa kwa Herode, mwana wamkazi
wa Herodia anavina pamaso pa anthu ndipo anasangalatsa kwambiri.
7 Kotero Herode analonjeza ndi lumbiro kumupatsa chilichonse chimene
mwanayo angamupemphe. 8 Ndipo atamupangira amayi ake anati,
"Mundipatse pomwe pano mutu wa Yohane M'batizi m'mbale."
9 Mfumuyo inamva chisoni koma chifukwa cha lumbiro lake ndi al-
endo amene anali pa phwando lake analamulira kuti chofuna chake
chipatsidwe; 10 ndipo anakadula mutu wa Yohane m'ndende. 11 Mutu
wake anawubweretsa m'mbale ndi kumupatsa mtsikanayo amene
anawutengera kwa amayi ake. 12 Ophunzira a Yohane anabwera nadza-
tenga mtembo wake ndi kukawuyika m'manda. Pomwepo iwo anapita
kukamuwuza Yesu.

### *Yesu Adyetsa Anthu 5,000*

13 Yesu atamva zimene zinachitika, anachoka pa bwato mwachinsinsi
kupita kumalo a yekha. Magulu a anthu atamva izi anamutsatira Iye
poyenda pansi kuchokera ku mizinda. 14 Yesu atafika ku mtunda, ndi

kuona gulu lalikulu la anthu, Iye anamva nawo chifundo ndipo anachiritsa
odwala awo.
15 Kutayamba mdima, ophunzira anabwera kwa Iye nati, "Kuno ndi
kutchire ndipo kwayamba kale kuda. Awuzeni anthu azipita kuti afike
ku midzi ndi kukadzigulira zakudya."
16 Yesu anawayankha kuti, "Sikofunika kuti azipita. Inuyo muwapatse
kanthu kuti adye."
17 Iwo anayankha kuti, "Tili ndi malofu asanu okha a buledi ndi nsomba
ziwiri."
18 Koma Iye anati, "Bweretsani kwa Ine." 19 Analamula anthu kuti
akhale pansi pa udzu ndipo anatenga buledi musanu ndi nsomba ziwiri
nayang'ana kumwamba, nayamika nagawa bulediyo. Kenaka anapereka
bulediyo kwa ophunzira ake ndipo ophunzirawo anagawira anthu. 20 Onse
anadya nakhuta ndipo ophunzira anatola zotsalira ndi kudzaza madengu
khumi ndi awiri. 21 Chiwerengero cha amene anadya kupatulako amayi
ndi ana chinali pafupifupi amuna 5,000.

### *Yesu Ayenda pa Nyanja*

22 Nthawi yomweyo anawawuza ophunzira ake kuti alowe m'bwato
ndi kuti atsogole kupita kutsidya lina pamene Iye ankawuza anthu kuti
azipita kwawo. 23 Atatha kuwawuza kuti azipita kwawo, Iye anakwera
ku phiri yekha kukapemphera. Pamene kumada anali kumeneko yekha.
24 Pamenepo n'kuti bwato litapita patali pang'ono kuchokera ku mtunda
ndipo linavutika ndi mafunde chifukwa mphepo inkawomba mokumana
nalo.
25 Pa ora lachinayi usiku, Yesu anabwera kwa iwo akuyendabe pa
nyanja. 26 Ophunzira atamuona akuyenda pa nyanja, anaopa nati, "Ndi
mzukwa!" Ndipo analira chifukwa cha mantha.
27 Koma Yesu nthawi yomweyo anawawuza kuti, "Limbani mtima!
Ndine, musaope."
28 Petro anayankha nati, "Ambuye ngati ndinu, mundiwuze ndibwere
kuli inuko pa madzipo."
29 Iye anati, "Bwera."
Pamenepo Petro anatuluka m'bwato ndipo anayenda pa madzi kupita
kwa Yesu. 30 Koma ataona mphepo, iye anachita mantha ndipo anayamba
kumira, nafuwula nati, "Ambuye ndipulumutseni!"
31 Ndipo mofulumira Yesu anatambasula dzanja lake namugwira iye,
nati, "Iwe wachikhulupiriro chochepa, bwanji unakayika?"
32 Ndipo atalowa m'bwato mphepo inaleka. 33 Pamenepo amene
anali m'bwato anamulambira Iye, nati, "Zoonadi, Inu ndinu Mwana wa
Mulungu."
34 Atawoloka, anafika ku Genesareti. 35 Anthu akumeneko ata-
muzindikira Yesu, iwo anatumiza mawu kwa onse ozungulira deralo. An-
thu anabwera ndi odwala awo onse kwa Iye. 36 Ndipo anamupempha alole
kuti akhudze mphonje ya mkanjo wake, ndipo onse amene anamukhudza
anachiritsidwa.

## 15

### *Miyambo ya Makolo*

1 Pamenepo Afarisi ena ndi aphunzitsi amalamulo anabwera kwa Yesu
kuchokera ku Yerusalemu ndipo anamufunsa kuti, 2 "Chifukwa chiyani

ophunzira anu amaphwanya mwambo wa akuluakulu? Iwo sasamba
m'manja pakudya!"

3 Yesu anayankha kuti, "Nanga chifukwa chiyani inu mumaphwanya
lamulo la Mulungu chifukwa cha mwambo wa makolo anu? 4 Pakuti
Mulungu anati, 'Lemekeza abambo ako ndi amayi ako' ndipo 'aliyense
amene atemberera abambo ake kapena amayi ake ayenera kuphedwa.'
5 Koma inu mumati, ngati munthu anena kwa abambo ake kapena
amayi ake kuti, 'Thandizo lililonse mukalirandira kuchokera kwa ine
ndi mphatso yoperekedwa kwa Mulungu,' 6 iye sakulemekeza nayo
abambo ake ndipo ndi khalidwe lotere inu mumapeputsa nalo Mawu a
Mulungu chifukwa cha mwambo wanu. 7 Inu anthu achiphamaso, Yesaya
ananenera za inu kuti,

8 " 'Anthu awa amandilemekeza Ine ndi milomo yawo,
koma mitima yawo ili kutali ndi Ine.
9 Amandilambira Ine kwachabe
ndi kuphunzitsa malamulo ndi malangizo a anthu.' "

10 Yesu anayitana gulu la anthu nati, "Mverani ndipo zindikirani.
11 Chimene chimalowa m'kamwa mwa munthu sichimuchititsa kukhala
woyipa, koma chimene chimatuluka m'kamwa mwake, icho ndi chimene
chimamuchititsa kukhala woyipa."

12 Pamenepo ophunzira anabwera kwa Iye ndipo anamufunsa kuti,
"Kodi mukudziwa kuti Afarisi anakhumudwa pamene anamva mawu
aja?"

13 Iye anayankha kuti, "Mbewu iliyonse imene Atate anga akumwamba
sanadzale idzazulidwa ndi mizu yomwe. 14 Alekeni, ndi atsogoleri
osaona. Ngati munthu wosaona atsogolera wosaona mnzake, onse awiri
adzagwera m'dzenje."

15 Petro anati, "Timasulireni fanizoli."

16 Yesu anawafunsa kuti, "Kani ngakhale inunso simumvetsa? 17 Kodi
inu simudziwa kuti chilichonse cholowa m'kamwa chimapita m'mimba
ndipo kenaka chimatuluka kunja kwa thupi? 18 Koma zinthu zimene zitu-
luka m'kamwa zimachokera mu mtima ndipo zimenezi zimamuchititsa
munthu kukhala woyipa. 19 Pakuti mu mtima mumatuluka maganizo
oyipa, zakupha, zachigololo, zadama, zakuba, zaumboni wonama ndi
zachipongwe. 20 Izi ndi zimene zimachititsa munthu kukhala woyipa;
koma kudya ndi m'manja mosasamba sikumuchititsa munthu kukhala
woyipa."

### *Mayi wa ku Kanaani*

21 Yesu atachoka kumalo amenewo anapita kudera la ku Turo ndi ku
Sidoni. 22 Mayi wa Chikanaani wochokera dera la komweko anabwera
kwa Iye akulira, nati, "Ambuye, Mwana wa Davide, ndichitireni chifundo!
Mwana wanga wamkazi akuzunzika kwambiri ndi chiwanda."

23 Yesu sanayankhe kanthu. Ndipo ophunzira ake anabwera namupem-
pha Iye kuti, "Muwuzeni achoke chifukwa akulira mofuwula pambuyo
pathu."

24 Iye anayankha kuti, "Ine ndinatumidwa kwa nkhosa zotayika za
Israeli zokha."

25 Mayiyo anabwera ndi kugwada pamaso pake, nati, "Ambuye
ndithandizeni!"

26 Iye anayankha kuti, "Sibwino kutenga chakudya cha ana ndi kupony-
era agalu."

27 Mayiyo anati, “Inde Ambuye. Komatu ngakhale agalu amadya
nyenyeswa zimene zimagwa kuchokera pa tebulo la mbuye wawo.”
28 Pomwepo Yesu anayankha kuti, “Mayi iwe uli ndi chikhulupiriro
chachikulu! Pempho lako lamveka.” Ndipo mwana wake wamkazi
anachira nthawi yomweyo.

### *Yesu Adyetsa Anthu 4,000*

29 Yesu anachoka kumeneko napita m’mbali mwa nyanja ya Galileya.
Ndipo anakwera ku phiri nakhala pansi. 30 Gulu lalikulu la anthu
linabwera kwa Iye ndi anthu olumala, osaona, ofa ziwalo, osayankhula ndi
ena ambiri nawagoneka pa mapazi ake ndipo Iye anawachiritsa. 31 Anthu
ataona osayankhula akuyankhula, ofa ziwalo akuchira, olumala miyendo
akuyenda ndi osaona akuona anadabwa kwambiri. Ndipo analemekeza
Mulungu wa Israeli.
32 Yesu anayitana ophunzira ake nati, “Ndili ndi chifundo ndi anthu awa;
akhala kale ndi Ine masiku atatu ndipo alibe chakudya. Ine sindifuna kuti
apite kwawo ndi njala chifukwa angakomoke pa njira.”
33 Ophunzira anayankha kuti, “Ndikuti kumene tingakapeze buledi
m’tchire muno okwanira kudyetsa gulu lotere?”
34 Yesu anawafunsa kuti, “Muli ndi malofu a buledi angati?”
Iwo anayankha kuti, “Asanu ndi awiri ndi tinsomba pang’ono.”
35 Iye anawuza gululo kuti likhale pansi. 36 Kenaka anatenga malofu
asanu ndi awiri aja ndi tinsombato ndipo atayamika anagawa napatsa
ophunzira ake ndipo iwo anagawira anthuwo. 37 Onse anadya ndipo
anakhuta. Pomaliza ophunzira anatolera zotsalira nadzaza madengu
asanu ndi awiri. 38 Chiwerengero cha anthu amene anadya chinali 4,000
kupatula amayi ndi ana. 39 Yesu atatha kuwuza gululo kuti lipite kwawo,
analowa m’bwato ndipo anapita kudera la Magadala.

# 16

### *Afarisi ndi Asaduki Afuna Chizindikiro*

1 Afarisi ndi Asaduki anabwera kwa Yesu ndi kumuyesa pomufunsa kuti
awaonetse chizindikiro chochokera kumwamba.
2 Iye anayankha kuti, “Kunja kukamada, inu mumati, kudzakhala
nyengo yabwino popeza thambo ndi lofiira. 3 Ndipo mmawa mumati,
‘Lero kudzakhala mvula yamphepo popeza thambo ndi lofiira ndi mita-
mbo ya mvula.’ Inu mumadziwa kutanthauzira maonekedwe a thambo
koma simungathe kutanthauzira zizindikiro za nthawi. 4 M’bado woyipa
ndi wachigololo umafuna chizindikiro chodabwitsa koma palibe ngakhale
chimodzi chidzapatsidwa kupatula chizindikiro cha Yona.” Pamenepo
Yesu anawasiya nachoka.

### *Yisiti wa Afarisi ndi Asaduki*

5 Koma atawoloka nyanja, ophunzira anayiwala kutenga buledi. 6 Yesu
anawawuza kuti, “Chenjerani, khalani tcheru ndi yisiti wa Afarisi ndi
Asaduki.”
7 Iwo anakambirana pakati pawo za izi ndipo anati, “Ichi n’chifukwa
chakuti sitinatenge buledi aliyense.”
8 Yesu atadziwa zokambirana zawo, anawafunsa kuti, “Chifukwa chiyani
mukukambirana zakuti, ‘mulibe buledi?’ Inu achikhulupiriro chochepa.
9 Kodi inu simukumvetsetsabe? Kodi simukukumbukira za buledi
musanu amene anadya anthu 5,000 ndi madengu amene munadzaza?

10 Kapena buledi musanu ndi muwiri amene anadya anthu 4,000, nanga
ndi madengu angati amene munadzaza? 11 Zitheka bwanji kuti inu
simukumvetsetsa kuti Ine sindinkayankhula nanu za buledi? Koma inu
chenjerani ndi yisiti wa Afarisi ndi Asaduki.” 12 Kenaka iwo anazindikira
kuti Iye samawawuza kuti achenjere ndi yisiti wa buledi koma ndi
chiphunzitso cha Afarisi ndi Asaduki.

### *Petro Avomereza za Yesu*

13 Yesu atafika ku chigawo cha Kaisareya Filipo, Iye anafunsa ophunzira
ake kuti, “Kodi anthu amati Mwana wa Munthu ndi ndani?”

14 Iwo anayankha kuti, “Ena amati ndi Yohane M’batizi; ena amati ndi
Eliya; komanso ena amati Yeremiya kapena mmodzi wa aneneri.”

15 Iye anafunsa kuti, “Nanga inuyo mumati ndine yani?”

16 Simoni Petro anayankha kuti, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa
Mulungu wamoyo.”

17 Yesu anati kwa iye, “Ndiwe wodala Simoni mwana wa Yona, popeza
si munthu amene anakuwululira izi koma Atate anga akumwamba.
18 Ndipo Ine ndikuwuza iwe kuti ndiwe Petro ndipo pa thanthwe ili Ine
ndidzamangapo mpingo wanga ndipo makomo a ku gehena sadzawu-
gonjetsa. 19 Ine ndidzakupatsa makiyi a Ufumu wakumwamba, ndipo
chilichonse chimene iwe udzachimanga pansi pano chidzamangidwanso
kumwamba.” 20 Pamenepo Iye anachenjeza ophunzira ake kuti asawuze
wina aliyense kuti ndi Khristu.

### *Yesu Aneneratu za Imfa Yake*

21 Kuyambira nthawi imeneyo Yesu anayamba kuwafotokozera ophun-
zira ake kuti Iye ayenera kupita ku Yerusalemu ndi kukazunzidwa
kwambiri m’manja mwa akulu a ansembe ndi aphunzitsi amalamulo kuti
ayenera kuphedwa, ndi kuti tsiku lachitatu adzaukitsidwa.

22 Petro anamutengera Iye pambali nayamba kumudzudzula kuti,
“Dzichitireni chifundo Ambuye, sizingachitike kwa Inu ayi.”

23 Yesu anatembenuka nati kwa Petro, “Choka pamaso panga Satana!
Iwe ndi chokhumudwitsa kwa Ine; iwe suganizira zinthu za Mulungu
koma zinthu za anthu.”

### *Za Kusenza Mtanda*

24 Pamenepo Yesu anati kwa ophunzira ake, “Ngati wina aliyense
abwera pambuyo panga ayenera kudzikana ndi kutenga mtanda wake
ndi kunditsata Ine. 25 Pakuti aliyense amene afuna kupulumutsa moyo
wake adzawutaya koma aliyense amene ataya moyo wake chifukwa cha
Ine adzawupeza. 26 Kodi munthu adzapindula chiyani ngati atapeza zonse
za dziko lapansi nataya moyo wake? Kapena munthu angapereke chiyani
chosinthana ndi moyo wake? 27 Pakuti Mwana wa Munthu adzabwera mu
ulemerero wa Atate ake ndi angelo ake ndipo pamenepo Iye adzapereka
mphotho kwa munthu mofanana ndi zimene anachita.

28 “Ine ndikuwuzani inu choonadi, ena amene akuyimirira pano
sadzalawa imfa asanaone Mwana wa Munthu akudza mu ufumu.”

## 17

### *Maonekedwe Aulemerero a Yesu pa Phiri*

1 Patapita masiku asanu ndi limodzi Yesu anatenga Petro, Yakobo, ndi
Yohane m’bale wa Yakobo pa okha ndipo anakwera nawo pa phiri lalitali.

2 Pamenepo Iye anasinthika maonekedwe ake pamaso pawo. Nkhope yake
inawala ngati dzuwa ndipo zovala zake zinayera kuti mbuu. 3 Nthawi
yomweyo Mose ndi Eliya anaonekera kwa iwo akuyankhulana ndi Yesu.

4 Petro anati kwa Yesu, "Ambuye ndi bwino kuti ife tikhale pano. Ngati
mufuna ndidzamanga misasa itatu umodzi wanu, wina wa Mose ndi wina
wa Eliya."

5 Iye akuyankhulabe, mtambo owala unawaphimba, ndipo mawu ochok-
era mu mtambo anati, "Uyu ndiye Mwana wanga amene ndimukonda
ndipo ndikondwera naye kwambiri. Mumumvere Iye!"

6 Ophunzira atamva zimenezi, anachita mantha nagwa pansi chafufu-
mimba. 7 Ndipo Yesu anabwera nawakhudza nati, "Dzukani, musaope."
8 Atayang'ana, sanaone wina aliyense kupatula Yesu yekha.

9 Akutsika ku phiriko, Yesu anawalamula kuti, "Musawuze wina aliyense
zimene mwaona, mpaka Mwana wa Munthu ataukitsidwa kwa akufa."

10 Ophunzira anamufunsa Iye kuti, "Nanga n'chifukwa chiyani aphunz-
itsi amalamulo amati Eliya ayenera kukhala woyamba kubwera?"

11 Yesu anayankha kuti, "Kunena zoona, Eliya adzayenera kubwera
ndipo adzakonza zinthu zonse. 12 Koma Ine ndikuwuzani inu kuti
Eliya anabwera kale koma iwo sanamuzindikire ndipo anachita naye
chilichonse chimene anafuna. Momwemonso iwo adzazunza Mwana
wa Munthu." 13 Pamenepo ophunzira anazindikira kuti amawawuza za
Yohane M'batizi.

### *Yesu Achiritsa Wodwala Matenda Akugwa*

14 Atafika ku gulu la anthu, munthu wina anamuyandikira Yesu ndi
kugwada pamaso pake. 15 Iye anati, "Ambuye, muchitireni chifundo
mwana wanga akudwala matenda akugwa ndipo akuvutika kwambiri.
Kawirikawiri iye amagwa pa moto kapena m'madzi. 16 Ine ndinabwera
naye kwa ophunzira anu koma alephera kumuchiritsa."

17 Yesu anayankha nati, "Haa, m'bado wosakhulupirira ndi wokhota
maganizo! Kodi ndidzakhala nanu mpaka liti? Ndidzapirira nanu
mpaka liti? Bwera nayeni kwa Ine mnyamatayo." 18 Yesu anadzudzula
chiwandacho ndipo chinatuluka mwa mnyamatayo ndipo anachira nthawi
yomweyo.

19 Pamenepo ophunzira anabwera kwa Yesu mwamseri ndi kumufunsa
kuti, "Chifukwa chiyani ife tinalephera kutulutsa chiwandacho?"

20 Iye anayankha kuti, "Chifukwa inu muli ndi chikhulupiriro
chaching'ono. Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti ngati muli ndi
chikhulupiriro monga kambewu ka mpiru, mukhoza kunena ndi phiri ili
kuti, 'Choka apa nupite apo,' ndipo lidzachoka. Palibe kanthu kamene
kadzakukanikani. 21 Chiwanda cha mtundu uwu sichingachoke chabe
koma ndi pemphero ndi kusala kudya."

### *Yesu Anena za Imfa yake Kachiwiri*

22 Atasonkhana pamodzi ku Galileya, Iye anawawuza kuti, "Mwana wa
Munthu akupita kukaperekedwa m'manja mwa anthu. 23 Iwo adzamupha
koma pa tsiku lachitatu adzaukitsidwa." Ndipo ophunzira anadzazidwa
ndi chisoni.

### *Yesu Apereka Msonkho*

24 Yesu ndi ophunzira ake atafika ku Kaperenawo, wolandira msonkho
wa ku Nyumba ya Mulungu anabwera kwa Petro namufunsa kuti, “Kodi
aphunzitsi anu sapereka msonkho wa Nyumba ya Mulungu?”
25 Iye anayankha kuti, “Inde amapereka.”
Petro atalowa m’nyumba, Yesu ndiye anayamba kuyankhula. Ndipo
anamufunsa kuti, “Ukuganiza bwanji Simoni, kodi mafumu a dziko lapansi
amalandira msonkho kuchokera kwa ana awo kapena kwa ena?”
26 Petro anayankha kuti, “Kuchokera kwa ena.”
Yesu ananena kwa iye kuti, “Ndiye kuti ana sapereka.” 27 Koma
kuti ife tisawakhumudwitse pita ku nyanja kaponye mbedza yako.
Katenge nsomba imene ukayambe kuyikola; kayitsekule kukamwa ndipo
ukapezamo ndalama. Katenge ndalamayo ndi kukapereka msonkho
wanga ndi wanu.

# 18

*Wamkulu mu Ufumu Wakumwamba*

1 Pa nthawi imeneyo ophunzira anabwera kwa Yesu ndipo anamufunsa
kuti, “Wamkulu woposa onse ndani mu ufumu wakumwamba?”
2 Iye anayitana kamwana kakang’ono ndi kukayimiritsa pakati pawo.
3 Ndipo Iye anati, “Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti ngati simusintha
ndi kukhala ngati tiana tating’ono, simudzalowa konse mu ufumu
wakumwamba. 4 Chifukwa chake, aliyense amene adzichepetsa yekha
ngati kamwana aka, ameneyo ndiye wamkulu koposa onse mu ufumu
wakumwamba. 5 Ndipo aliyense amene alandira kamwana kakang’ono
ngati aka mu dzina langa, alandira Ine.

*Za Kuchimwitsa Ena*

6 “Koma ngati wina aliyense achimwitsa mmodzi wa ana awa, amene
akhulupirira Ine, kuti achimwe, kukanakhala bwino kuti iye aman-
giriridwe chimwala chachikulu m’khosi mwake ndi kumizidwa pansi pa
nyanja. 7 Tsoka dziko lapansi chifukwa cha zinthu zimene ziyenera
kubwera, koma tsoka kwa munthu amene abweretsa zotere! 8 Ngati
dzanja lako kapena phazi lako likuchimwitsa, lidule ndi kulitaya. Ndi
bwino kwa iwe kulowa m’moyo wosatha wolumala kusiyana ndi kukhala
ndi manja awiri kapena mapazi awiri ndi kukaponyedwa ku moto
wosatha. 9 Ndipo ngati diso lako likuchimwitsa, ulichotse ndi kulitaya. Ndi
bwino kwa iwe kuti ukalowe ku moyo wosatha ndi diso limodzi kuposa
ndi kukhala ndi maso awiri ndi kukaponyedwa ku moto wa gehena.”

*Fanizo la Nkhosa Yotayika*

10 “Onetsetsani kuti musanyoze mmodzi wa anawa. Pakuti ndikuwuzani
kuti angelo awo kumwamba amakhala pamaso pa Atate anga akumwamba
nthawi zonse.” 11 (Mwana wa Munthu anabwera kudzapulumutsa
chimene chinatayika).
12 “Kodi mukuganiza bwanji? Ngati munthu ali ndi nkhosa 100 ndipo
imodzi n’kusowa, kodi sasiya 99 zija m’mapiri ndi kupita kukafuna imodzi
yosocherayo? 13 Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti akayipeza amasangalala
kwambiri chifukwa cha nkhosa imodziyo kuposa nkhosa 99 zimene
sizinasochere. 14 Chimodzimodzinso Atate anu akumwamba safuna kuti
mmodzi wa anawa atayike.

*Za M’bale Amene Akuchimwirani*

15 “Ngati m’bale wako akuchimwira, pita kamuwuze cholakwa chake
pa awiri. Ngati akumvera, wamubweza m’bale wakoyo. 16 Koma
ngati sakumvera, katenge wina mmodzi kapena ena awiri, ‘kuti nkhani
itsimikizike ndi umboni wa anthu awiri kapena atatu.’ 17 Ngati iye
akana kuwamvera iwo, kaneneni ku mpingo; ndipo ngati sakamvera
ngakhale mpingo, muchite naye monga mukanachitira ndi wakunja
kapena wolandira msonkho.

18 “Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti chilichonse chimene muchimanga
pa dziko lapansi, chidzamangidwanso kumwamba, ndipo chilichonse
chimene muchimasula pa dziko chidzamasulidwanso kumwamba.

19 “Komanso ndikukuwuzani inu kuti ngati awiri a inu pa dziko
lapansi avomerezana kanthu kalikonse kamene mukapempha, Atate anga
akumwamba adzakuchitirani. 20 Pakuti pamene awiri kapena atatu
asonkhana pamodzi m’dzina langa, Ine ndili nawo pomwepo.”

### *Fanizo la Wantchito Wopanda Chifundo*

21 Kenaka Petro anabwera kwa Yesu ndi kumufunsa kuti, “Ambuye, kodi
m’bale wanga akandichimwira ndimukhululukire kokwanira kangati?
Mpaka kasanu n’kawiri?”

22 Yesu anayankha kuti, “Ine ndikukuwuza iwe kuti osati kasanu
n’kawiri, koma ka 70 kuchulukitsa ndi kasanu n’kawiri.

23 “N’chifukwa chake, ufumu wakumwamba ukufanana ndi mfumu
imene inafuna kuti antchito ake abweze ngongole. 24 Atangoyamba
kulandira, anamubweretsa munthu kwa iye amene anakongola ndalama
10,000. 25 Popeza sakanatha kubweza, bwanayo analamula kuti iye, mkazi
wake, ana ake ndi zonse anali nazo zigulitsidwe kuti zibweze ngongoleyo.

26 “Wantchitoyo anagwada pamaso pake namupempha iye kuti, ‘Lez-
ereni mtima ndipo ndidzabweza zonse.’ 27 Bwana wakeyo anamuchitira
chifundo, namukhululukira ngongoleyo ndipo anamulola apite.

28 “Koma wantchito uja atatuluka, anakumana ndi wantchito mnzake
amene anakongola kwa iye madinari 100. Anamugwira, nayamba ku-
mukanyanga pa khosi, namuwumiriza nati, ‘Bwezere zimene unakongola
kwa ine!’

29 “Wantchito mnzakeyo anagwada namupempha iye kuti, ‘Lezere
mtima ine, ndipo ndidzakubwezera.’

30 “Koma iye anakana. M’malo mwake, anachoka nakamumangitsa
kufikira atabweza ngongoleyo. 31 Pamene antchito ena anaona zomwe
zinachitikazo, anamva chisoni kwambiri ndipo anapita nakawuza bwana
wawo zonse zimene zinachitika.

32 “Pamenepo bwanayo anayitana wantchitoyo nati, ‘Iwe wantchito
woyipa mtima, ndinakukhululukira ngongole yako yonse chifukwa
unandipempha. 33 Kodi iwe sukanamuchitira chifundo wantchito mnzako
monga momwe ine ndinakuchitira iwe?’ 34 Ndi mkwiyo, bwana wakeyo
anamupereka kwa oyang’anira ndende kuti amuzuze mpaka atabweza
zonse zimene anakongola.

35 “Umu ndi mmene Atate anga akumwamba adzachitira ndi aliyense
wa inu ngati simukhululukira m’bale wanu ndi mtima wonse.”

## 19

### *Za Kuthetsa Ukwati*

1 Yesu atatsiriza kunena zinthu zimenezi, anachoka ku Galileya ndi
kupita ku chigawo cha Yudeya mbali ina ya mtsinje wa Yorodani. 2 Magulu
akulu a anthu anamutsatira Iye, ndipo iwo anachiritsidwa pomwepo.
3 Afarisi ena anabwera kwa Iye kudzamuyesa. Anamufunsa Iye nati,
“Kodi ndikololedwa kuti mwamuna amuleke mkazi wake pa chifukwa
china chilichonse?”
4 Iye anayankha kuti, “Kodi simunawerenge kuti pachiyambi Mulungu
analenga iwo, ‘mwamuna ndi mkazi?’ 5 Ndipo anati, ‘Pa chifukwa ichi
mwamuna adzasiya abambo ake ndi amayi ake nakaphatikana ndi mkazi
wake, ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi.’ 6 Motero salinso awiri
ayi koma mmodzi. N’chifukwa chake chimene Mulungu wachimanga
pamodzi munthu wina asachilekanitse.”
7 Ndipo iwo anamufunsa nati, “Nanga n’chifukwa chiyani Mose anala-
mula kuti mwamuna azipatsa mkazi wake kalata ya chisudzulo ndi
kumuchotsa?”
8 Yesu anayankha kuti, “Mose anakulolezani kuti muzisudzula akazi anu
chifukwa cha kuwuma mitima kwanu. Koma sizinali chotere kuyambira
pachiyambi. 9 Ine ndikuwuzani kuti aliyense amene asudzula mkazi
wake, osati chifukwa cha chiwerewere nakakwatira mkazi wina, achita
chigololo.”
10 Ophunzira ake anati kwa Iye, “Ngati umu ndi mmene zilili pa
mwamuna ndi mkazi, kuli bwino kusakwatira.”
11 Yesu anayankha kuti, “Si aliyense amene angavomere chiphunzitso
ichi, koma kwa okhawo amene achimvetsetsa. 12 Pakuti ena ndi akuti
sangakwatire chifukwa anabadwa motero, ena ali motero chifukwa
chofulidwa ndi anthu ndipo ena anawukana ukwati chifukwa cha ufumu
wakumwamba. Iye amene angalandire ichi alandire.”

### *Yesu Adalitsa Ana*

13 Pamenepo anabwera nawo ana kwa Yesu kuti awasanjike manja ndi
kuwapempherera. Koma ophunzira ake anadzudzula amene anabweretsa
anawo.
14 Yesu anati, “Lolani ana abwere kwa Ine, ndipo musawaletse pakuti
ufumu wakumwamba ndi wa iwo onga anawa.” 15 Atasanjika manja ake
pa anawo, anachokapo.

### *Mnyamata Wolemera ndi Ufumu wa Mulungu*

16 Taonani mnyamata wina anabwera kwa Yesu namufunsa kuti,
“Aphunzitsi, ndi chinthu chiti chabwino chimene ndiyenera kuchita kuti
ndipeze moyo wosatha?”
17 Yesu anayankha kuti, “Ukundifunsiranji Ine za chinthu chimene ndi
chabwino? Pali mmodzi yekha amene ndi wabwino. Ngati ukufuna
kulowa m’moyo wosatha mvera malamulo.”
18 Mnyamatayo anamufunsa kuti, “Ndi ati?”
Yesu anayankha kuti, “Usaphe, usachite chigololo, usabe, usapereke
umboni onama, 19 lemekeza abambo ako ndi amayi ako ndipo konda
mnansi wako monga iwe mwini.”
20 Mnyamatayo anati, “Zonsezi ndimazisunga, nanga chatsala ndi
chiyani?”
21 Yesu anayankha kuti, “Ngati ukufuna kukhala wangwiro, pita
kagulitse katundu wako ndi kupereka kwa osauka, ndipo udzakhala ndi
chuma kumwamba. Ukakachita zimenezi, ukabwere udzanditsate Ine.”

22 Mnyamatayo atamva zimenezi, anachoka mokhumudwa, chifukwa
anali ndi chuma chambiri.
23 Pamenepo Yesu anati kwa ophunzira ake, “Zoonadi, ndikuwuzani kuti
n’kovuta kuti olemera akalowe mu ufumu wakumwamba. 24 Komanso
ndikuwuzani kuti, n’kwapafupi kuti ngamira idzere pa kabowo ka zingano
kusiyana ndi kuti wolemera akalowe mu ufumu wa Mulungu.”
25 Ophunzira atamva zimenezi, anadabwa kwambiri ndipo anamufunsa
kuti, “Nanga angapulumuke ndani?”
26 Yesu anawayang’ana iwo nati, “Ndi anthu, izi n’zosatheka, koma ndi
Mulungu zinthu zonse zimatheka.”
27 Petro anamuyankha Iye kuti, “Ife tinasiya zonse ndi kukutsatirani Inu!
Nanga tsono ife tidzalandira chiyani?”
28 Yesu anawawuza kuti, “Zoonadi, ndikuwuzani kuti pa nthawi yokon-
zanso zinthu zonse, pamene Mwana wa Munthu adzakhala pa mpando
wake waufumu mu ulemerero wake kumwamba, inu amene mwanditsata
Ine mudzakhalanso pa mipando khumi ndi iwiri yaufumu, kuweruza
mafuko khumi ndi awiri a Israeli. 29 Ndipo aliyense amene wasiya
nyumba, kapena abale, kapena alongo, kapena bambo kapena mayi
kapena mkazi, kapena ana, kapena minda chifukwa cha Ine adzalandira
madalitso ochuluka ndi kulandiranso moyo wosatha. 30 Koma ambiri
amene ali oyambirira adzakhala omalizira, ndipo ambiri amene ndi
omalizira adzakhala oyambirira.”

# 20

*Fanizo la Aganyu M’munda wa Mphesa*

1 “Ufumu wakumwamba uli ngati mwini munda amene anapita mmawa
kukalemba anthu aganyu kuti akagwire ntchito m’munda wake wa mpesa.
2 Anagwirizana kuwalipira dinari monga malipiro a tsiku limodzi ndipo
anawatumiza m’munda wake wamphesa.
3 “Nthawi 9 koloko mmawa, anatulukanso naona ena atayimirira pa
msika akungokhala. 4 Anawawuza kuti, ‘Inunso pitani mukagwire ntchito
m’munda wanga wa mpesa, ndipo ndidzakulipirani malipiro oyenera.’
5 Ndipo anapita.
“Anatulukanso nthawi ya 12 koloko masana, ndi nthawi ya 3 koloko
masananso nachita chimodzimodzi. 6 Nthawi ya 5 koloko madzulo
anatulukanso ndipo anapeza enanso atangoyimirira. Anawafunsa kuti,
‘Chifukwa chiyani mukungoyimirira pano tsiku lonse osagwira ntchito?’
7 “Iwo anayankha kuti, ‘Chifukwa palibe munthu amene watilemba
ganyu.’
“Iye anawawuza kuti, ‘Inunso pitani mukagwire ntchito m’munda
wanga wa mpesa.’
8 “Ndipo pofika madzulo, mwini munda wamphesa anayitana kapitawo
wake nati, ‘Itana antchito ndipo uwapatse malipiro awo, kuyambira
omalizira aja mpaka oyamba.’
9 “Antchito amene anawalemba ganyu pa 5 koloko masana anafika ndipo
aliyense analandira dinari. 10 Ndipo atabwera kwa amene analembedwa
poyamba anayembekezera kuti alandira zambiri. Koma aliyense wa
iwo analandira dinari. 11 Atalandira, anayamba kuderera kwa mwini
mundayo. 12 Iwo anati, ‘Anthu amene munawalemba pomalizira agwira

ntchito ora limodzi, ndipo mwawafananitsa ndi ife amene tathyoka nayo
ntchito ndi kutentha kwa dzuwa tsiku lonse.'
13 "Koma iye anamuyankha mmodzi wa iwo nati, 'Bwenzi, ine sikuti
sindinachite chilungamo. Kodi sunavomereze kuti ugwira ntchito ndi
kulandira dinari? 14 Tenga malipiro ako pita. Ndikufuna kumupatsa
munthu amene ndinamulemba pomaliza mofanana ndi mmene ndaku-
patsira iwe. 15 Kodi ndilibe ufulu wochita zimene ndikufuna ndi ndalama
zanga? Kapena ukuyipidwa chifukwa ndine wopereka mowolowamanja?'
16 "Momwemo omalizira adzakhala oyamba ndipo oyamba adzakhala
omalizira."

### *Yesu Anenanso za Imfa Yake*

17 Tsopano pamene Yesu ankapita ku Yerusalemu, anatengera pam-
bali ophunzira ake khumi ndi awiriwo nati kwa iwo, 18 "Tikupita ku
Yerusalemu, ndipo Mwana wa Munthu adzaperekedwa kwa akulu a
ansembe ndi aphunzitsi amalamulo. Iwo adzamuweruza kuti aphedwe,
19 ndipo adzamupereka kwa anthu a mitundu ina kuti amunyoze ndi
kumukwapula ndi kumupachika. Pa tsiku lachitatu adzaukitsidwa!"

### *Pempho la Mkazi wa Zebedayo*

20 Amayi a ana a Zebedayo anabwera ndi ana ake kwa Yesu, nagwada
pansi namupempha Iye.
21 Yesu anawafunsa kuti, "Mukufuna chiyani?"
Amayiwo anati, "Lolani kuti ana anga awiriwa adzakhale mmodzi ku
dzanja lanu lamanja ndi wina ku dzanja lanu lamazere mu ufumu wanu."
22 Yesu anawawuza kuti, "Simukudziwa chimene mukupempha. Kodi
mungathe kumwera chikho chimene ndidzamwera Ine?"
Iwo anayankha nati, "Inde tingathe."
23 Yesu anawawuza kuti, "Zoonadi mudzamwera chikho changa, koma
kuti mudzakhale ku dzanja langa lamanja kapena lamazere si kwa Ine
kupereka. Malo awa ndi a iwo amene anakonzeredweratu ndi Atate anga."
24 Ophunzira khumi aja, anawapsera mtima abale awiriwo. 25 Yesu
anawayitana onse pamodzi nati, "Mukudziwa kuti olamulira a mitundu
ina ali ndi mphamvu pa iwo, ndipo akuluakulu awo amawalamulira.
26 Siziyenera kutero ndi inu. M'malo mwake, aliyense amene akufuna
kukhala wamkulu pakati panu akhale wotumikira wanu. 27 Ndipo aliyense
amene akufuna kukhala woyamba akhale kapolo wanu. 28 Momwenso
Mwana wa Munthu sanabwere kudzatumikiridwa, koma kudzatumikira,
ndi kupereka moyo wake kukhala dipo la anthu ambiri."

### *Yesu Achiritsa Anthu Awiri Osaona*

29 Pamene Yesu ndi ophunzira ake ankachoka ku Yeriko, gulu lalikulu la
anthu linawatsata. 30 Amuna awiri osaona anakhala m'mbali mwa msewu,
ndipo pamene anamva kuti Yesu akudutsa anafuwula kuti, "Ambuye,
Mwana wa Davide, tichitireni chifundo!"
31 Gulu la anthulo linawadzudzula iwo ndi kuwawuza kuti akhale
chete, koma anafuwulitsabe kuti, "Ambuye, Mwana wa Davide, tichitireni
chifundo!"
32 Yesu anayima ndi kuwayitana ndipo anawafunsa kuti, "Mukufuna
ndikuchitireni chiyani?"
33 Anamuyankha nati, "Ambuye, tikufuna tione!"
34 Yesu anamva nawo chifundo ndipo anakhudza maso awo. Nthawi
yomweyo anaona namutsata Iye.

# 21

*Yesu Alowa mu Yerusalemu*

1 Akuyandikira ku Yerusalemu anafika ku Betifage pa phiri la Olivi,
Yesu anatumiza ophunzira awiri, 2 nawawuza kuti, "Pitani ku mudzi
uli patsogolo panu, ndipo mukakangolowa m'menemo mukapeza bulu
womangidwa ali ndi mwana pa mbali pake. Mukawamasule ndipo
mubwere nawo kwa Ine. 3 Wina akakayankhula, mukamuwuze kuti
Ambuye akuwafuna, ndipo adzawatumiza nthawi yomweyo."

4 Izi zinachitika kukwaniritsa zimene zinayankhulidwa ndi mneneri:

5 "Uza mwana wamkazi wa Ziyoni,
taona, mfumu yako ikubwera kwa iwe,
yofatsa ndi yokwera pa bulu,
pa kamwana ka bulu, mwana wa nyama yonyamula katundu."

6 Ophunzirawo anapita nachita monga Yesu anawalamulira.
7 Anabweretsa bulu ndi mwana wake, nayala zovala zawo pa abuluwo,
ndipo Yesu anakwerapo. 8 Gulu lalikulu la anthu linayala zovala zawo
mu msewu pamene ena anadula nthambi zamitengo ndi kuziyala mu
msewumo. 9 Magulu amene anali patsogolo pake ndi amene amamutsatira
anafuwula kuti,

"Hosana Mwana wa Davide!"

"Wodala Iye amene abwera m'dzina la Ambuye!"

"Hosana mmwambamwamba!"

10 Yesu atalowa mu Yerusalemu, mzinda wonse unatekeseka ndipo anthu
anafunsa kuti, "Ndani ameneyu?"

11 Magulu a anthu anayankha kuti, "Uyu ndi Yesu, mneneri wochokera
ku Nazareti."

*Yesu m'Nyumba ya Mulungu*

12 Yesu analowa m'dera lina la Nyumba ya Mulungu ndipo anatulutsa
kunja anthu onse amene ankachita malonda. Anagubuduza matebulo a
osinthira ndalama ndi mipando ya ogulitsa nkhunda. 13 Iye anawawuza
kuti, "Zinalembedwa kuti Nyumba yanga idzatchedwa Nyumba ya
mapemphero koma inu mwayisandutsa phanga la anthu achifwamba."

14 Anthu osaona ndi olumala anabwera kwa Iye m'Nyumba ya Mu-
lungu ndipo anawachiritsa. 15 Koma akulu a ansembe ndi aphunzitsi
amalamulo ataona zodabwitsa zimene anachita, komanso ana akufuwula
m'Nyumbayo kuti, "Hosana kwa Mwana wa Davide," anapsa mtima.

16 Anamufunsa kuti, "Kodi mukumva zimene anawa akunena?"

Yesu anayankha nati, "Inde. Kodi simunawerenge kuti,

"Kuchokera m'kamwa mwa ana ndi makanda
mwatuluka mayamiko?"

17 Ndipo anawasiya natuluka mu mzindawo ndi kupita ku Betaniya,
kumene anakagona.

*Yesu Atemberera Mtengo wa Mkuyu*

18 Mmamawa, pamene amabwera ku mzinda, anamva njala. 19 Ataona
mtengo wamkuyu m'mbali mwa msewu, anapitapo koma sanapeze
kanthu koma masamba okhaokha. Pamenepo anati kwa mtengowo,
"Usadzabalenso chipatso!" Nthawi yomweyo mtengowo unafota.

20 Ophunzira ataona zimenezi, anadabwa nafunsa kuti, “Kodi mtengo
wamkuyuwu wauma msanga bwanji?”
21 Yesu anayankha kuti, “Zoonadi, ndikuwuzani kuti ngati muli ndi
chikhulupiriro ndipo simukayika, simudzangochita zokha zachitika kwa
mkuyuzi, koma mudzatha kuwuza phiri ili kuti, ‘Pita, kadziponye wekha
m’nyanja,’ ndipo zidzachitikadi. 22 Ngati mukhulupirira, mudzalandira
chilichonse chimene muchipempha m’pemphero.”

*Amufunsa Yesu za Ulamuliro Wake*

23 Yesu analowa m’Nyumba ya Mulungu, ndipo pamene ankaphunzitsa,
akulu a ansembe ndi akuluakulu anabwera kwa Iye namufunsa kuti,
“Muchita izi ndi ulamuliro wanji ndipo anakupatsani ndani ulamuliro
umenewu?”
24 Yesu anayankha kuti, “Inenso ndikufunsani funso limodzi,
mukandiyankha, Inenso ndikukuwuzani ndi ulamuliro wa yani umene
ndikuchitira izi. 25 Ubatizo wa Yohane unachokera kuti? Kumwamba
kapena kwa anthu?”
Anakambirana pakati pawo ndipo anati, “Tikati, ‘Kuchokera
kumwamba,’ Iye adzafunsa kuti, ‘Bwanji simunakhulupirire?’ 26 Koma
tikati, ‘Kuchokera kwa anthu,’ ife tikuopa anthuwa, pakuti onse
amakhulupirira kuti Yohane anali mneneri.”
27 Choncho anamuwuza Yesu kuti, “Sitikudziwa.”
Pamenepo Iye anati, “Inenso sindikuwuzani kuti ndi ulamuliro wa yani
umene ndichitira izi.”

*Fanizo la Ana Amuna Awiri*

28 “Kodi muganiza bwanji? Panali munthu wina anali ndi ana aamuna
awiri. Anapita kwa woyamba nati, ‘Mwanawe pita kagwire ntchito lero
m’munda wamphesa.’
29 “Iye anayankha kuti, ‘Sindipita,’ koma pambuyo pake anasintha
maganizo napita.
30 “Kenaka abambowo anapita kwa mwana winayo nanena chimodzi-
modzi. Iye anayankha kuti, ‘Ndipita abambo,’ koma sanapite.
31 “Ndani wa awiriwa anachita chimene abambo ake amafuna?”
Anamuyankha nati, “Woyambayo.”
Yesu anawawuza kuti, “Ndikuwuzani zoonadi, kuti amisonkho ndi
adama akulowa mu ufumu wa Mulungu inu musanalowemo.” 32 Pakuti
Yohane anabwera kwa inu kuti akuonetseni njira yachilungamo,
koma inu simunakhulupirire iye, koma amisonkho ndi adama ana-
mukhulupirira. Koma ngakhale munaona izi, simunatembenuke mtima
ndi kumukhulupirira iye.

*Fanizo la Alimi*

33 “Tamverani fanizo lina: Panali mwini munda amene anadzala
mphesa. Anamanga mpanda kuzungulira mundawo, nakumba mopon-
deramo mphesa ndipo anamanga nsanja. Kenaka anabwereketsa munda
wamphesawo kwa alimi ena napita pa ulendo. 34 Pamene nthawi yokolola
inakwana, anatumiza antchito ake kwa matenanti aja kuti akatenge
zipatso zake.
35 “Alimi aja anagwira antchito ake; namenya mmodzi, napha wina,
ndi kumuponya miyala wachitatuyo. 36 Kenaka anatumiza antchito
ena oposa oyambawo ndipo matenantiwo anawachitira chimodzimodzi.
37 Pomalizira anatumiza mwana wake. Anati adzamuchitira ulemu
mwana wanga.

[38] “Koma alimiwo ataona mwanayo anati kwa wina ndi mnzake, ‘Uyu
ndiye olowa m’malo mwa abambo ake. Tiyeni timuphe ndipo titenge
cholowa chake.’ [39] Pamenepo anamutenga namuponyera kunja kwa
munda wamphesa namupha.
[40] “Tsono akabwera mwini munda wamphesa adzachita nawo chiyani
matenantiwo?”
[41] Iwo anayankha kuti, “Adzawapha moyipa alimi oyipawo ndipo
adzabwereketsa mundawo kwa alimi ena amene adzamupatsa gawo lake
la mbewu pa nthawi yokolola.”
[42] Yesu anawawuza kuti, “Kodi simunawerenge m’malemba kuti:
“ ‘Mwala umene omanga nyumba anawukana,
womwewo wasanduka mwala wofunika kwambiri wa pa ngodya.
Ambuye wachita izi,
ndipo ndi zodabwitsa m’maso mwathu.’
[43] “N’chifukwa chake ndi kukuwuzani kuti ufumu wa Mulungu udza-
landidwa kwa inu ndipo udzapatsidwa kwa anthu amene adzabereka
chipatso chake. [44] Amene agwa pa mwalawu adzadukaduka, ndipo amene
udzamugwere udzamuthudzula.”
[45] Akulu a ansembe ndi Afarisi atamva mafanizo a Yesu, anadziwa
kuti ankanena iwo. [46] Pamenepo anafuna njira yoti amugwirire, koma
anaopa gulu la anthu chifukwa anthu onse ankakhulupirira kuti Iye anali
mneneri.

# 22

*Fanizo la Phwando la Ukwati*

[1] Yesu anayankhula nawonso m’mafanizo, nati, [2] “Ufumu wakumwamba
uli ngati mfumu imene inakonzera phwando mwana wake wamwamuna.
[3] Anatumiza antchito ake kwa amene anayitanidwa kuphwando koma
anakana kubwera.
[4] “Kenaka anatumiza antchito ena nati, ‘Awuzeni oyitanidwa kuti
phwando lakonzedwa: ndapha ng’ombe yayimuna ndi nyama zina
zonenepa ndipo zonse zakonzedwa. Bwerani ku phwando laukwati.’
[5] “Koma iwo sanalabadire ndipo anachoka; wina anapita ku munda
wake ndi wina ku malonda ake. [6] Ndipo otsalawo anagwira antchito ake,
nawazunza ndi kuwapha. [7] Mfumu inakwiya. Inatumiza asilikali ake
ndipo anawononga opha anzawowo ndi kutentha mzinda wawo.
[8] “Pamenepo anati kwa antchito ake, ‘Phwando laukwati lakonzedwa,
koma amene ndinawayitana sanali oyenera. [9] Pitani ku mphambano za
misewu ndipo kayitaneni aliyense amene mukamupeze kuti abwere ku
phwando.’ [10] Pamenepo antchitowo anapita ku misewu nakasonkhanitsa
anthu onse amene anakawapeza, abwino ndi oyipa omwe, ndipo nyumba
ya madyerero inadzaza ndi oyitanidwa.
[11] “Koma pamene mfumu inabwera kudzaona oyitanidwawo, inaona
munthu amene sanavale zovala zaukwati. [12] Inamufunsa kuti, ‘Bwenzi
walowa bwanji muno wopanda zovala zaukwati?’ Munthuyo anakhala
chete.
[13] “Pamenepo mfumuyo inawuza otumikira kuti, ‘M’mangeni manja ndi
miyendo, ndipo muponyeni kunja, ku mdima kumene kudzakhale kulira
ndi kukuta mano.’
[14] “Popeza oyitanidwa ndi ambiri koma osankhidwa ndi ochepa.”

*Za Kupereka Msonkho*

15 Kenaka Afarisi anatuluka nakakonza njira zomupezera zifukwa Yesu
m'mawu ake. 16 Anatumiza ophunzira awo kwa Iye pamodzi ndi Aherodia.
Anati, "Aphunzitsi, tidziwa kuti ndinu wangwiro ndi kuti mumaphunzitsa
mawu a Mulungu monga mwa choonadi. Simutekeseka ndi anthu, popeza
simusamala kuti kodi ndi ndani? 17 Tiwuzeni tsono maganizo anu ndi
otani, kodi n'kololedwa kupereka msonkho kwa Kaisara kapena ayi?"
18 Koma Yesu podziwa maganizo awo oyipa anati, "Inu achiphamaso,
bwanji mufuna kundipezera chifukwa? 19 Onetseni ndalama imene
mumapereka msonkho." Iwo anabweretsa dinari, 20 ndipo anawafunsa
kuti, "Kodi chithunzi ichi ndi malemba awa ndi za ndani?"
21 Iwo anayankha kuti, "Ndi za Kaisara."
Pamenepo anawawuza kuti, "Perekani kwa Kaisara zake za Kaisara, ndi
kwa Mulungu zake za Mulungu."
22 Atamva izi, anadabwa, ndipo anamusiya Iye, nachoka.

### *Ukwati ndi za Kuuka kwa Akufa*

23 Tsiku lomwelo Asaduki amene amati kulibe za kuukanso, anabwera
kwa Iye ndi funso. 24 Iwo anati, "Aphunzitsi, Mose anatiwuza kuti
munthu akamwalira wosasiya ana, m'bale wake akuyenera kukwatira
mkazi wamasiyeyo kuti amuberekere ana m'bale wakeyo. 25 Tsopano
panali abale asanu ndi awiri pakati pathu. Woyambayo anakwatira ndipo
anamwalira, ndipo popeza analibe ana, m'bale wake analowa chokolo.
26 Izi zinachitikiranso m'bale wa chiwiri ndi wachitatu mpaka wachisanu
ndi chiwiri. 27 Pa mapeto pake mkaziyo anamwaliranso. 28 Tsopano,
kodi akadzaukitsidwa adzakhala mkazi wa ndani mwa asanu ndi awiriwa
popeza aliyense anamukwatirapo?"
29 Yesu anayankha kuti, "Inu mukulakwitsa chifukwa simukudziwa
malemba kapena mphamvu ya Mulungu. 30 Anthu akadzaukitsidwa,
sadzakwatira kapena kukwatiwa; adzakhala ngati angelo kumwamba.
31 Koma za kuukitsidwa kwa akufa, kodi simunawerenge zimene Mulungu
ananena kwa inu kuti, 32 'Ine ndine Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa
Isake ndi Mulungu wa Yakobo?' Iyeyo si Mulungu wa akufa koma wa
amoyo."
33 Magulu a anthu atamva zimenezi, anazizwa ndi chiphunzitso chake.

### *Lamulo Lalikulu Koposa*

34 Pakumva kuti Yesu anawakhalitsa chete Asaduki, Afarisi anasonkhana
pamodzi. 35 Mmodzi wa iwo, katswiri wa malamulo anamuyesa Iye
ndi funso ndipo anati, 36 "Aphunzitsi, kodi lamulo lalikulu koposa mu
malamulo ndi liti?" 37 Yesu anayankha kuti, "Uzikonda Yehova Mulungu
wako ndi mtima wako wonse ndi moyo wako wonse ndi nzeru zako zonse.
38 Ili ndi lamulo loyamba ndi loposa onse. 39 Ndipo lachiwiri ndi lofanana
nalo: 'Konda mnansi wako monga iwe mwini.' 40 Malamulo onse ndi
aneneri zakhazikika pa malamulo awiriwa."

### *Kodi Khristu ndi Mwana wa Ndani?*

41 Afarisi atasonkhana pamodzi, Yesu anawafunsa kuti, 42 "Kodi muku-
ganiza bwanji za Khristu? Ndi Mwana wa ndani?"
Iwo anayankha kuti, "Mwana wa Davide."
43 Iye anawawuza kuti, "Nanga zikutheka bwanji kuti Davide poy-
ankhula mwa Mzimu Woyera amatchula Iye 'Ambuye?' Pakuti akuti,
44 "Ambuye anati kwa Ambuye wanga:
'Khala pa dzanja langa lamanja

mpaka ndiyike adani ako
pansi pa mapazi ako.'
45 Ngati tsono Davide amamutchula 'Ambuye,' zingatheke bwanji kukhala
mwana wake?" 46 Panalibe wina anatha kuyankha, ndipo kuchokera
pamenepo, panalibe wina anayerekeza kumufunsa funso.

# 23

### *Yesu Adzudzula Aphunzitsi Amalamulo ndi Afarisi*

1 Pamenepo Yesu anati kwa magulu a anthu ndi ophunzira ake:
2 "Aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi amakhala pa mpando wa Mose.
3 Choncho muziwamvera ndi kuchita chilichonse chimene akuwuzani.
Koma musachite zimene amachita, popeza sachita zimene amaphunzitsa.
4 Amamanga akatundu olemera nawayika pa mapewa a anthu, koma iwo
eni safuna kuwanyamula.
5 "Ntchito zawo amachita ndi cholinga chakuti anthu awaone. Amadzimangirira timaphukusi tikulutikulu ta Mawu a Mulungu pa mphumi ndi
pa mkono komanso amatalikitsa mphonje za mikanjo yawo. 6 Amakonda
malo aulemu pa maphwando ndi malo ofunika kwambiri m'masunagoge.
7 Amakondwera ndi kupatsidwa moni m'misika ndi kutchulidwa kuti
'Aphunzitsi.'
8 "Koma inu simuyenera kutchulidwa 'Aphunzitsi,' popeza muli naye
Mbuye mmodzi ndipo inu nonse ndinu abale. 9 Ndipo musamatchule wina
aliyense pansi pano kuti 'Atate,' pakuti muli ndi Atate mmodzi, ndipo
ali kumwamba. 10 Komanso musamatchedwenso 'Mtsogoleri,' pakuti
muli naye Mtsogoleri mmodzi amene ndi Khristu. 11 Wamkulu pakati
panu adzakhala wokutumikirani. 12 Pakuti aliyense amene adzikuza
adzachepetsedwa, ndipo aliyense amene adzichepetsa adzakuzidwa.

### *Tsoka kwa Aphunzitsi Amalamulo ndi Afarisi*

13 "Tsoka kwa inu aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi achiphamaso!
Mumatseka pa khomo la kumwamba kuti anthu asalowemo. Eni akenu
simulowamo komanso simulola kuti ena amene akufuna kulowa kuti
alowe. 14 Muli ndi tsoka, inu aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi, anthu
achiphamaso! Mumawadyera akazi amasiye chuma chawo, kwinaku
n'kumanamizira kunena mapemphero ataliatali. Chifukwa cha zimenezi
Mulungu adzakulangani koposa.
15 "Tsoka kwa inu, aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi, achiphamaso!
Mumayenda maulendo ambiri pa mtunda ndi pa nyanja kuti mutembenuze munthu mmodzi, ndipo akatembenuka, mumamusandutsa kukhala
mwana wa gehena kawiri kuposa inu.
16 "Tsoka kwa inu, atsogoleri akhungu! Mumati, 'Ngati wina alumbira
kutchula Nyumba ya Mulungu, zilibe kanthu; koma ngati wina alumbira
kutchula ndalama zagolide za m'Nyumbayo, wotere ayenera kusunga
lumbiro lake.' 17 Inu akhungu opusa! Chopambana n'chiyani: ndalama
zagolide, kapena Nyumba imene imayeretsa golideyo? 18 Ndiponso
mumati, 'Ngati wina alumbira kutchula guwa lansembe, sizitanthauza
kanthu; koma ngati wina alumbira kutchula mphatso ya paguwa
lansembe, wotere ayenera kusunga lumbiro lake.' 19 Inu anthu akhungu!
Chopambana n'chiyani: mphatso, kapena guwa limene limayeretsa
mphatsoyo? 20 Chifukwa chake, iye amene alumbira kutchula guwa
alumbira pa ilo ndi pa chilichonse chili pamenepo. 21 Ndipo iye wolumbira

potchula Nyumba ya Mulungu alumbira pa Nyumbayo ndi pa Iye amene
amakhala m'menemo. 22 Ndipo iye wolumbira kutchula kumwamba
alumbira kutchula mpando waufumu wa Mulungu ndi pa Iye wokhalapo.
23 "Tsoka kwa inu, aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi, achiphamaso!
Mumapereka chakhumi cha timbewu tonunkhira ndi cha timbewu
tokometsera chakudya. Koma mwasiya zofunikira kwambiri za
m'malamulo monga chilungamo, chifundo ndi kukhulupirika. Muyenera
kuchita zomalizirazi komanso osasiya zoyambazo. 24 Atsogoleri akhungu
inu! Mumachotsa kantchentche mu chakumwa chanu koma mumameza
ngamira.
25 "Tsoka kwa inu, aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi achiphamaso!
Mumayeretsa kunja kwa chikho ndi mbale, koma m'katimo mwadzaza
ndi dyera ndi kusadziretsa. 26 Afarisi akhungu! Poyamba tsukani m'kati
mwa chikho ndi mbale, ndipo kunja kwake kudzakhalanso koyera.
27 "Tsoka kwa inu, aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi, achiphamaso!
Muli ngati ziliza pa manda zowala kunja zimene zimaoneka zokongola
koma m'katimo mwadzaza mafupa a anthu akufa ndi zonyansa zina zonse.
28 Chimodzimodzinso, kunja mumaoneka kwa anthu kuti ndinu olungama
koma m'katimo ndinu odzaza ndi chinyengo ndi zoyipa zina.
29 "Tsoka kwa inu, aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi, achiphamaso! Mu-
mamanga ziliza za aneneri ndi kukongoletsa manda a olungama. 30 Ndipo
mumati, 'Ngati tikanakhala m'masiku a makolo athu sitikanakhetsa nawo
magazi a aneneri.' 31 Potero mukutsimikiza kuti muli ana a iwo amene
anapha aneneri. 32 Dzazani inu muyeso wa uchimo wa makolo anu!
33 "Njoka inu! Ana amamba! Mudzachithawa bwanji chilango cha
gehena? 34 Choncho ndi kutumizirani aneneri ndi anthu anzeru ndi
aphunzitsi. Ena a iwo mudzawapha ndi kuwapachika; ena mudzawak-
wapula m'masunagoge anu ndi kuwafunafuna kuchokera mudzi wina
kufikira wina. 35 Ndipo magazi onse a olungama amene anakhetsedwa
pansi pano, kuyambira magazi a Abele, olungama kufikira Zakariya
mwana wa Barakiya, amene munamupha pakati pa Nyumba ya Mulungu
ndi guwa lansembe, adzakhala pa inu. 36 Zoonadi, ndikuwuzani kuti
zonsezi zidzafika pa m'bado uno.
37 "Haa! Yerusalemu, Yerusalemu, iwe amene umapha aneneri ndi
kugenda miyala amene atumidwa kwa iwe, kawirikawiri ndimafuna
kusonkhanitsa ana ako, monga nkhuku imasonkhanitsira ana ake pansi
pa mapiko ake, koma iwe sunafune. 38 Taona, nyumba yako yasiyidwa
ya bwinja. 39 Chifukwa chake ndikuwuza kuti simudzandionanso kufikira
pamene mudzati, 'Wodala Iye amene akudza m'dzina la Ambuye.' "

# 24

*Zizindikiro za Masiku Otsiriza*

1 Yesu anatuluka m'Nyumba ya Mulungu ndipo akuchoka ophun-
zira ake anadza kwa Iye ndi kumuonetsa mamangidwe a Nyumbayo.
2 Iye anawafunsa kuti, "Kodi mukuona zinthu zonsezi? Zoonadi, Ine
ndikuwuzani kuti palibe mwala pano umene udzasiyidwe pa unzake;
uliwonse udzagwetsedwa pansi."
3 Pamene Yesu anakhala pansi pa phiri la Olivi, ophunzira ake anabwera
kwa Iye mwamseri nati, "Tiwuzeni, kodi izi zidzachitika liti, ndipo

chizindikiro cha kubwera kwanu ndi zizindikiro za kutha kwa dziko
zidzakhala chiyani?”
4 Yesu anayankha kuti, “Onetsetsani kuti wina asakunyengeni. 5 Pakuti
ambiri adzabwera m’dzina langa nadzati, ‘Ndine Khristu,’ ndipo
adzanyenga ambiri. 6 Mudzamva za nkhondo ndi mbiri za nkhondo,
koma onetsetsani kuti musadzidzimuke nazo. Zotere ziyenera kuchitika,
koma chimaliziro sichinafike. 7 Mtundu ndi mtundu udzawukirana,
ndipo ufumu ndi ufumu udzawukirana. Kudzakhala njala ndi zivomerezi
m’malo osiyanasiyana. 8 Zonsezi ndi chiyambi chabe cha zowawa.
9 “Pamenepo adzakuperekani kuti mukazunzidwe ndi kuphedwa, ndipo
mitundu yonse idzakudani chifukwa cha Ine. 10 Pa nthawi imeneyo
ambiri adzasiya chikhulupiriro ndipo adzadana ndi kuperekana wina
ndi mnzake, 11 ndipo aneneri onama ambiri adzaoneka ndi kunyenga
anthu ambiri. 12 Chifukwa cha kuchuluka kwa zoyipa, chikondi cha
ambiri chidzazirala, 13 koma wopirira kufikira chimaliziro adzapulumuka.
14 Ndipo uthenga wa ufumu udzalalikidwa ku dziko lonse lapansi ngati
umboni kwa mitundu yonse, ndipo pomwepo chimaliziro chidzafika.”
15 “Tsono mukadzaona chinthu chonyansa chosakaza chitayima pamalo
oyera chimene anayankhula mneneri Danieli, owerengayo azindikire.
16 Pamenepo amene ali ku Yudeya athawire ku mapiri. 17 Yemwe
ali pa denga la nyumba yake asatsike kukatulutsa chinthu chilichonse
m’nyumba. 18 Yemwe ali ku munda asapite kukatenga mkanjo wake.
19 Kudzakhala koopsa kwambiri masiku amenewo kwa amayi oyem-
bekezera ndi kwa oyamwitsa! 20 Pempherani kuti kuthawa kwanu
kusadzachitike nthawi yozizira kapena pa Sabata. 21 Popeza kudzakhala
masautso aakulu, omwe safanana ndi ena ali onse chiyambireni cha
dziko lapansi mpaka lero lino ndipo sadzafanananso ndi ena. 22 Ngati
masiku amenewo sakanafupikitsidwa, palibe mmodzi akanapulumuka,
koma chifukwa cha osankhidwawo masiku amenewo adzafupikitsidwa.
23 Pa nthawi imeneyo ngati wina adzati kwa inu, ‘Onani, Khristu ali pano!’
Kapena, ‘Uyo ali ukoyo!’ Musakhulupirire. 24 Chifukwa akhristu onama
ndi aneneri onama adzaoneka ndipo adzachita zizindikiro zazikulu ndi
zodabwitsa kuti akanyenge ngakhale osankhidwawo ngati kukanakhala
kotheka kutero. 25 Onani, ndakuwuzani izi nthawi isanafike.
26 “Ndiye ngati wina akuwuzani inu kuti, ‘Uyo ali ku chipululu,’
inu musapiteko; kapena akati, ‘Uyu ali kuno m’chipinda cham’kati,’
musakhulupirire. 27 Monga momwe mphenzi ing’anima kuchokera
kummawa kupita kumadzulo, momwemonso kudzakhala kubwera kwa
Mwana wa Munthu. 28 Kulikonse kuli chinthu cha kufa, makwangwala
adzasonkhanako.
29 “Akadzangotha mavuto a masiku amenewo,

“ ‘dzuwa lidzadetsedwa,
ndipo mwezi sudzawala;
nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba,
ndipo mphamvu za mmwamba zidzagwedezeka.’

30 “Pa nthawi imeneyo chizindikiro cha Mwana wa Munthu chidzaoneka
mlengalenga, ndipo mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzalira. Idzaona
Mwana wa Munthu akubwera ndi mitambo, mphamvu ndi ulemerero
waukulu. 31 Ndipo adzatuma angelo ake, ndi kulira kwa lipenga
kwakukulu, nadzasonkhanitsa osankhidwa ake kuchokera ku mphepo
zinayi, ndi kuchokera kumathero a thambo kufika mbali ina.

32 “Tsopano kuchokera ku mtengo wamkuyu phunzirani ichi: Pamene
uyamba kuphukira, masamba ake akatuluka, mumadziwa kuti dz-
inja layandikira. 33 Momwemonso, pamene mudzaona zinthu zonsezi
mudzadziwe kuti ali pafupi pa khomo penipeni. 34 Zoonadi, ndikuwuzani
kuti m’bado uwu sudzatha mpaka zinthu zonse zitachitika. 35 Kumwamba
ndi dziko lapansi zidzatha, koma mawu anga sadzatha.”

### *Tsiku ndi Nthawi Sizidziwika*

36 “Palibe amene adziwa za tsikulo kapena nthawi, angakhale angelo
akumwamba, angakhale Mwana, koma Atate okha. 37 Monga momwe
zinalili nthawi ya Nowa, momwemonso zidzatero pobwera kwa Mwana
wa Munthu. 38 Pakuti masiku amenewo chisanafike chigumula, anthu
amadya ndi kumwa, kukwatira ndi kukwatiwa, mpaka tsiku limene Nowa
analowa m’chombo; 39 ndipo sanadziwe za chimene chikanachitika mpaka
pamene chigumula chinafika ndi kuwamiza onse. Umu ndi mmene
zidzakhalira pobwera kwa Mwana wa Munthu. 40 Amuna awiri adzakhala
m’munda; wina adzatengedwa ndi wina adzatsala. 41 Amayi awiri
adzakhala akusinja pa mtondo; wina adzatengedwa ndi wina adzatsala.

42 “Chifukwa chake yang’anirani, popeza simudziwa tsiku lanji limene
Ambuye anu adzabwera. 43 Koma zindikirani ichi: Ngati mwini nyumba
akanadziwa nthawi yanji ya usiku imene mbala imabwera, sakanagona
ndipo sakanalola kuti nyumba yake ithyoledwe. 44 Inunso tsono muyenera
kukhala okonzeka, chifukwa Mwana wa Munthu adzabwera pa nthawi
imene inu simukumuyembekezera.

### *Wantchito Wokhulupirika ndi Wosakhulupirika*

45 “Kodi wantchito wokhulupirika ndi wanzeru amene ambuye ake
anamuyika kukhala woyang’anira antchito a m’nyumba kuti awapatse
chakudya chawo pa nthawi yake ndani? 46 Chidzakhala chabwino kwa
wantchitoyo ngati mbuye wake pofika adzamupeza akuchita zimenezi.
47 Zoonadi, ndikuwuzani kuti adzamuyika kukhala woyang’anira katundu
wake yense. 48 Koma tiyerekeze kuti wantchitoyo ndi woyipa, nati kwa
iye yekha, ‘Mbuye wanga akuchedwa kubwera,’ 49 nayamba kumenya
antchito anzake, nadya ndi kumwa ndi zidakwa. 50 Mbuye wa wantchitoyo
adzabwera pa tsiku limene iye samamuyembekezera ndi pa nthawi imene
iye sakuyidziwa. 51 Adzamulanga koopsa ndipo adzamuyika kokhala
anthu achiphamaso, kumene kudzakhala kulira ndi kukukuta mano.”

## 25

### *Fanizo la Anamwali Khumi*

1 “Nthawi imeneyo ufumu wakumwamba udzafanizidwa ndi anamwali
khumi amene anatenga nyale zawo napita kukakumana ndi mkwati.
2 Asanu anali opusa ndipo asanu ena anali ochenjera. 3 Opusawo anatenga
nyale zawo koma sanatenge mafuta; 4 koma ochenjerawo anatenga mafuta
awo m’mabotolo pamodzi ndi nyale zawo. 5 Mkwati anachedwa ndipo
onse anayamba kusinza nagona.

6 “Pakati pa usiku kunamveka kufuwula kuti, ‘Onani Mkwati! Tulukani
kuti mukakumane naye!’

7 “Pamenepo anamwali onse anadzuka nayatsa nyale zawo. 8 Opusawo
anati kwa ochenjerawo, ‘Tipatseniko mafuta anu; nyale zathu zikuzima.’

9 “Ochenjerawo anayankha, nati, ‘Ayi sangakwanire inu ndi ife. Pitani
kwa ogulitsa mafuta ndi kukadzigulira nokha.’

10 “Koma pamene ankapita kukagula mafutawo, mkwati anafika.
Anamwali amene anali okonzeka aja analowa naye pamodzi m’nyumba
ya phwando la ukwati. Ndipo khomo linatsekedwa.

11 “Pambuyo pake enawo anabwera nati, ‘Ambuye! Ambuye! Titsekulireni!’

12 “Koma iye anayankha kuti, ‘Zoonadi, ine ndikuwuzani kuti sindikukudziwani.’

13 “Choncho khalani odikira, popeza simudziwa tsiku kapena nthawi.”

### *Fanizo la Kagwiritsidwe Ntchito ka Ndalama*

14 “Komanso udzafanizidwa ndi munthu amene ankapita pa ulendo,
ndipo anayitana antchito ake nawasiyira chuma chake. 15 Wina anamu-
patsa ndalama 5,000, kwa wina 2,000 ndi kwa wina 1,000. Aliyense monga
mwa nzeru zake. Pamenepo anapita pa ulendo wake. 16 Munthu amene
analandira ndalama 5,000 uja, anapita nthawi yomweyo nachita nazo
malonda napindula 5,000 zina. 17 Chimodzimodzinso amene analandira
2,000 uja anapindula 2,000 zina. 18 Koma munthu amene analandira 1,000
uja, anapita nakumba dzenje nabisapo ndalama ya mbuye wake.

19 “Patapita nthawi yayitali, mbuye wa antchitowo anabwera nawayi-
tana kuti afotokoze chimene anachita ndi ndalama zija. 20 Munthu amene
analandira ndalama 5,000 uja anabweretsa 5,000 zina nati, ‘Ambuye
munandisungitsa 5,000, taonani ndapindula 5,000 zinanso.’

21 “Ambuye ake anayankha nati, ‘Wachita bwino, wantchito wabwino
ndi wokhulupirika iwe! Wakhala wokhulupirika pa zinthu zochepa;
ndidzakuyika iwe kukhala woyang’anira zinthu zambiri. Bwera, udza-
kondwere pamodzi ndi mbuye wako!’

22 “Munthu amene anali ndi ndalama 2,000 uja anabweranso nati,
‘Ambuye munandisungitsa 2,000, onani, ndapindula 2,000 zinanso.’

23 “Mbuye wake anayankha nati, ‘Wachita bwino, wantchito wabwino
ndi wokhulupirika! Wakhala wokhulupirika pa zinthu zochepa; ndidza-
kuyika kukhala woyang’anira zinthu zambiri. Bwera, udzakondwere
pamodzi ndi mbuye wako!’

24 “Kenaka munthu amene analandira ndalama 1,000 uja anabw-
era nati, ‘Ambuye ndinadziwa kuti ndinu munthu wowuma mtima,
amene mumakolola pamene simunadzale ndi kututa kumene simunafese.
25 Choncho ndinachita mantha ndipo ndinapita ndi kukabisa ndalama
yanuyo pa dzenje. Onani, si iyi ndalama yanu ija.’

26 “Mbuye wake anayankha nati, ‘Iwe wantchito woyipa ndi waulesi!
Iwe umadziwa kuti ndimakolola pamene sindinadzale, ndi kututa kumene
sindinafese. 27 Bwanji sunayike ndalama yanga kwa osunga ndalama
kuti ine pobwera ndidzalandire ndalama yangayo pamodzi ndi chiwon-
goladzanja?

28 “ ‘Mulandeni ndalamayo, ndipo patsani iye amene ali ndi ndalama
10,000. 29 Pakuti aliyense amene ali nazo adzapatsidwa zambiri, ndipo
adzakhala nazo zochuluka. Aliyense amene alibe adzalandidwa ngakhale
chimene ali nacho. 30 Ndipo muponyeni wantchito wopanda phinduyu
kunja, ku mdima kumene kudzakhala kulira ndi kukukuta mano.’ ”

### *Nkhosa ndi Mbuzi*

31 “Pamene Mwana wa Munthu adzabwera mu ulemerero wake,
pamodzi ndi angelo ake onse, adzakhala pa mpando waufumu mu
ulemerero wakumwamba. 32 Mitundu yonse ya anthu idzasonkhanitsidwa
pamaso pake, ndipo adzawalekanitsa iwo wina ndi mnzake monga m’busa
amalekanitsa nkhosa ndi mbuzi. 33 Adzayika nkhosa ku dzanja lake
lamanja ndi mbuzi ku lamanzere.
34 “Pamenepo mfumu idzati kwa a ku dzanja lamanja, ‘Bwerani inu
odalitsika ndi Atate anga; landirani ufumu umene unakonzedwa chifukwa
cha inu kuyambira pachiyambi cha dziko. 35 Pakuti ndinali ndi njala ndipo
munandipatsa chakudya, ndinali ndi ludzu ndipo munandipatsa madzi
akumwa, ndinali mlendo ndipo munandilandira, 36 ndinali wausiwa
ndipo munandiveka, ndinali wodwala ndipo munandisamalira, ndinali ku
ndende ndipo inu munandiyendera.’
37 “Ndipo olungamawo adzamuyankha kuti, ‘Ambuye ndi liti tinakuo-
nani muli ndi njala ndipo tinakudyetsani, kapena ludzu ndipo tinaku-
patsani madzi akumwa? 38 Ndi liti tinakuonani muli mlendo ndipo
tinakulandirani, kapena wa usiwa ndipo tinakuvekani? 39 Ndi liti
tinakuonani mutadwala kapena ku ndende ndipo tinakuyenderani?’
40 “Mfumu idzayankha kuti, ‘Zoonadi, ndikuwuzani kuti chilichonse
chimene munachitira mmodzi wa abale anga onyozekawa munandichitira
Ine.’
41 “Pamenepo adzanena kwa akumanzere kwake kuti, ‘Chokani kwa Ine,
inu otemberereredwa, pitani ku moto wosatha wokonzedwera mdierekezi
ndi angelo ake. 42 Pakuti ndinali ndi njala ndipo simunandipatse
chakudya, ndinali ndi ludzu ndipo simunandipatse madzi akumwa,
43 ndinali mlendo koma inu simunandilandire, ndinali wa usiwa
koma simunandiveke, ndinali wodwala komanso ku ndende simunan-
disamalire.’
44 “Iwo adzayankha kuti, ‘Ambuye ndi liti tinakuonani muli ndi njala
kapena ludzu kapena mlendo kapena wausiwa kapena wodwala kapena
m’ndende, ndipo kuti sitinakuthandizeni?’
45 “Iye adzayankha kuti, ‘Zoonadi, ndikuwuzani kuti chilichonse
chimene simunachitire mmodzi wa abale anga onyozekawa simunandi-
chitire Ine.’
46 “Amenewa adzapita ku chilango chosatha pamene olungama ku moyo
wosatha.”

## 26

*Chiwembu cha Ayuda pa Yesu*

1 Yesu atamaliza kuyankhula zonsezi, anati kwa ophunzira ake, 2 “Monga
mukudziwa, kwatsala masiku awiri kuti Paska ifike ndipo Mwana wa
Munthu adzaperekedwa kuti apachikidwe.”
3 Pamenepo akulu a ansembe ndi akuluakulu anasonkhana ku nyumba
ya mkulu wa ansembe dzina lake Kayafa, 4 ndipo anapangana kuti
amugwire Yesu mobisa ndi kumupha. 5 Ndipo anati, “Osati nthawi
yaphwando chifukwa pangabuke chipolowe pakati pa anthu.”

*Yesu Adzozedwa ku Betaniya*

6 Yesu ali ku Betaniya m’nyumba Simoni Wakhate, 7 mayi wina
anabwera kwa Iye ndi botolo la mafuta onunkhira a mtengowapatali,
amene anathira pa mutu pake Iye akudya pa tebulo.

8 Ophunzira ataona izi anayipidwa nafunsa kuti, “Chifukwa chiyani
akuwononga chotere? 9 Mafuta amenewa akanatha kugulitsidwa pa
mtengo waukulu, ndipo ndalama zake zikanaperekedwa kwa osauka.”
10 Yesu podziwa izi anawawuza kuti, “Chifukwa chiyani mukumuvutitsa
mayiyu? Wandichitira Ine chinthu chabwino. 11 Osauka mudzakhala
nawo nthawi zonse, koma simudzakhala ndi Ine nthawi zonse. 12 Pamene
wathira mafuta onunkhirawa pa thupi langa, wachita izi kukonzekera
kuyikidwa kwanga m’manda. 13 Zoonadi, ndikuwuzani kuti kulikonse
kumene Uthenga Wabwinowu udzalalikidwa ku dziko lonse lapansi,
zimene wachitazi zidzanenedwanso pomukumbukira.”

### *Yudasi Avomereza Kupereka Yesu*

14 Pamenepo mmodzi wa khumi ndi awiriwo wotchedwa Yudasi Isikar-
ioti anapita kwa akulu a ansembe 15 nafunsa kuti, “Kodi mundipatsa
chiyani ngati nditamupereka Iye kwa inu?” Pamenepo anamuwerengera
ndalama zokwanira masiliva makumi atatu. 16 Kuyambira pamenepo
Yudasi anafunafuna nthawi yabwino yoti amupereke Yesu.

### *Paska Womaliza ndi Mgonero wa Ambuye*

17 Pa tsiku loyamba laphwando la buledi wopanda yisiti, ophunzira
anabwera kwa Yesu ndi kumufunsa kuti, “Kodi mukufuna tikakonze kuti
malo odyera Paska?”
18 Iye anayankha kuti, “Pitani mu mzinda kwa munthu wakutiwakuti
ndipo kamuwuzeni kuti, ‘Aphunzitsi akuti, nthawi yanga yoyikidwa
yayandikira. Ine ndidzadya phwando la Paska ndi ophunzira anga ku
nyumba kwako.’ ” 19 Pamenepo ophunzira ake anachita monga momwe
Yesu anawawuzira ndipo anakonza Paska.
20 Kutada, Yesu ndi ophunzira ake khumi ndi awiriwo anakhala pa
tebulo n’kumadya. 21 Akudya, Iye anati, “Zoonadi, ndikuwuzani kuti
mmodzi wa inu adzandipereka.”
22 Iwo anamva chisoni kwambiri ndipo anayamba kuyankhulana naye
mmodzimmodzi nati, “Kodi n’kukhala ine Ambuye?”
23 Yesu anayankha nati, “Iye amene akusunsa m’mbale pamodzi ndi
Ine, yemweyo adzandipereka. 24 Mwana wa Munthu adzaphedwa monga
mmene kunalembedwera za Iye. Koma tsoka kwa munthu amene apereka
Mwana wa Munthu! Kukanakhala bwino kwa iye akanapanda kubadwa.”
25 Ndipo Yudasi amene anamupereka Iye anati, “Monga n’kukhala ine
Aphunzitsi?”
Yesu anayankha nati, “Iwe watero.”
26 Pamene ankadya, Yesu anatenga buledi, nayamika ndipo anamun-
yema nagawira ophunzira ake nanena kuti, “Tengani, idyani; ili ndi thupi
langa.”
27 Kenaka anatenga chikho, nayamika nachipereka kwa iwo nati,
“Imwani nonsenu. 28 Awa ndi magazi anga a pangano amene akhetsedwa
chifukwa cha ambiri kuti akhululukidwe machimo. 29 Ndikuwuzani kuti
sindidzamwanso kuchokera ku chipatso cha mtengo wa mpesa kuyambira
lero mpaka tsiku ilo pamene ndidzamwenso mwatsopano ndi inu mu
ufumu wa Atate anga.”
30 Atayimba nyimbo, anatuluka kupita ku phiri la Olivi.

### *Yesu Aneneratu kuti Petro Adzamukana*

31 Pamenepo Yesu anawawuza kuti, “Usiku omwe uno inu nonse
mudzandithawa, pakuti kwalembedwa:
“ ‘Kantha m’busa,
ndipo nkhosa zidzabalalika.’
32 Koma ndikadzauka, ndidzatsogola kupita ku Galileya.”
33 Petro anayankha nati, “Ngakhale onsewa atakuthawani, ine ndekha
ayi.”
34 Yesu anayankha nati, “Zoonadi, ndikukuwuza kuti usiku omwe uno,
asanalire tambala, udzandikana Ine katatu.”
35 Koma Petro ananenetsa nati, “Ngakhale kutakhala kufa nanu
pamodzi, sindidzakukanani.” Ndipo ophunzira onse ananena chimodzi-
modzi.

*Yesu mu Getsemani*

36 Kenaka Yesu anapita ku malo otchedwa Getsemani, ndipo anawawuza
kuti, “Khalani pano pamene Ine ndikukapemphera apo.” 37 Anatenga
Petro ndi ana awiri a Zebedayo, ndipo anayamba kumva chisoni ndi
kuvutika mu mtima. 38 Pamenepo anawawuza kuti, “Moyo wanga uli ndi
chisoni chofa nacho. Khalani pano ndipo dikirani pamodzi ndi Ine.”
39 Atapita patsogolo pang’ono, anagwa pansi chafufumimba napem-
phera kuti, “Atate anga, ngati ndikotheka, chikho ichi chichotsedwe kwa
Ine. Koma osati monga mmene ndifunira, koma monga mufunira Inu.”
40 Kenaka anabwera kwa ophunzira ake nawapeza ali mtulo. Iye
anafunsa Petro kuti, “Kodi anthu inu, simukanakhala maso pamodzi
ndi Ine kwa ora limodzi lokha? 41 Khalani maso ndi kupemphera kuti
musagwe m’mayesero. Mzimu ukufuna koma thupi ndi lofowoka.”
42 Anachokanso nakapemphera kachiwiri kuti, “Atate anga, ngati
chikhochi sichingandichoke, mpaka nditamwa, kufuna kwanu kuchitike.”
43 Atabweranso anawapeza ali mtulo chifukwa zikope zawo zi-
nalemedwa ndi tulo. 44 Choncho anawasiya napitanso kukapemphera
kachitatu nanenanso chimodzimodzi.
45 Kenaka anabwera kwa ophunzira ake nati kwa iwo, “Kodi mukanag-
onabe ndi kupumula? Taonani, ora layandikira ndipo Mwana wa Munthu
akuperekedwa m’manja mwa ochimwa. 46 Imirirani, tiyeni tizipita!
Wondipereka Ine wafika!”

*Amugwira Yesu*

47 Akuyankhula choncho, Yudasi mmodzi mwa khumi ndi awiriwo
anafika. Pamodzi ndi iye panali gulu lalikulu la anthu ali ndi
mikondo ndi zibonga otumidwa ndi akulu a ansembe ndi akuluakulu.
48 Womuperekayo anawawuziratu chizindikiro anthuwo kuti, “Amene
ndidzapsompsona ndi iyeyo; mugwireni.” 49 Pamenepo Yudasi anapita
kwa Yesu nati, “Moni, Aphunzitsi!” Ndipo anapsompsona Iye.
50 Yesu anayankha kuti, “Bwenzi langa, chita chimene wabwerera.”
Pamenepo anthuwo anabwera patsogolo namugwira Yesu ndi kumu-
manga. 51 Pa chifukwa ichi, mmodzi wa anzake a Yesu anagwira lupanga
lake, nalisolola ndi kutema wantchito wa mkulu wa ansembe, nadula
khutu lake.
52 Yesu anati kwa iye, “Bwezera lupanga lako m’chimake, chifukwa onse
amene amapha ndi lupanga adzafa ndi lupanga. 53 Kodi mukuganiza kuti
sindingathe kupempha Atate anga ndipo nthawi yomweyo n’kundipatsa

magulu a angelo oposa khumi ndi awiri? 54 Koma nanga malemba akwaniritsidwa bwanji amene akuti ziyenera kuchitika motere?"

55 Pa nthawi yomweyo Yesu anati kwa gululo, "Kodi ndine mtsogoleri wa anthu owukira kuti mwabwera ndi malupanga ndi zibonga kudzandigwira? Tsiku ndi tsiku ndimakhala m'Nyumba ya Mulungu kuphunzitsa, koma simunandigwire. 56 Koma zonsezi zachitika kuti zolembedwa ndi aneneri zikwaniritsidwe." Pamenepo ophunzira anamusiya nathawa.

### *Yesu ku Bwalo la Akulu Ayuda*

57 Iwo amene anamugwira Yesu anamutengera kwa Kayafa, mkulu wa ansembe, kumene aphunzitsi amalamulo ndi akuluakulu anasonkhana.
58 Koma Petro anamutsatira Iye patali, mpaka ku bwalo la mkulu wa ansembe. Analowa nakhala pansi pamodzi ndi alonda kuti aone zotsatira.

59 Akulu a ansembe ndi akulu olamulira Ayuda amafunafuna umboni wonama wofuna kuphera Yesu. 60 Koma sanathe kupeza uliwonse, angakhale kuti mboni zambiri zabodza zinapezeka.

Pomalizira mboni ziwiri zinabwera patsogolo. 61 Ndipo zinati, "Munthu uyu anati, 'Ndikhoza kupasula Nyumba ya Mulungu ndi kuyimanganso m'masiku atatu.' "

62 Pamenepo mkulu wa ansembe anayimirira nati kwa Yesu, "Kodi suyankha? Kodi umboni umenewu ndi otani umene anthu awa akupereka kukutsutsa Iwe?" 63 Koma Yesu anakhalabe chete.

Mkulu wa ansembe anati kwa Iye, "Ndikulamulira Iwe ndi lumbiro pamaso pa Mulungu wa Moyo: utiwuze ife ngati ndiwe Khristu Mwana wa Mulungu."

64 Yesu anayankha nati, "Mwanena ndinu. Koma ndikunena kwa inu nonse: m'tsogolomo mudzaona Mwana wa Munthu atakhala kudzanja lamanja la Wamphamvuzonse ndipo akubwera ndi mitambo ya kumwamba."

65 Pamenepo mkulu wa ansembe anang'amba zovala zake nati, "Wanyoza Mulungu! Tifuniranji mboni zina? Taonani, tsopano mwamva mwano wake. 66 Mukuganiza bwanji?"

Iwo anayankha kuti, "Ayenera kuphedwa!"

67 Kenaka anamulavulira kumaso namumenya ndi zibakera. Ena anamumenya makofi. 68 Ndipo anati, "Tanenera kwa ife, Khristu. Wakumenya ndani?"

### *Petro Amukana Yesu*

69 Tsopano Petro anakhala ku bwalo la nyumbayo, ndipo mtsikana wantchito anabwera kwa iye nati, "Iwenso unali ndi Yesu wa ku Galileya."

70 Koma iye anakana pamaso pawo nati, "Sindikudziwa chimene ukunena."

71 Kenaka anachoka kupita ku khomo la mpanda, kumene mtsikana wina anamuonanso nawuza anthu nati, "Munthu uyu anali ndi Yesu wa ku Nazareti."

72 Iye anakananso molumbira kuti, "Sindimudziwa munthuyu!"

73 Patapita kanthawi pang'ono, amene anayimirira pamenepo anapita kwa Petro nati, "Zoonadi, ndiwe mmodzi wa iwo, popeza mayankhulidwe ako akukuwulula."

74 Pamenepo anayamba kudzitemberera ndipo analumbira kwa iwo nati, "Sindimudziwa munthu ameneyo!"

Nthawi yomweyo tambala analira. 75 Ndipo Petro anakumbukira mawu
amene Yesu anayankhula kuti, "Tambala asanalire, udzandikana Ine
katatu." Ndipo anatuluka panja nakalira kwambiri.

# 27

### *Yudasi Adzimangirira*

1 Mmamawa, akulu a ansembe onse ndi akuluakulu anavomerezana
kuti aphe Yesu. 2 Anamumanga, napita naye kukamupereka kwa
bwanamkubwa Pilato.

3 Yudasi, amene anamupereka Iye, ataona kuti Yesu waweruzidwa
kuti akaphedwe, anatsutsika mu mtima mwake nakabweza ndalama
zamasiliva makumi atatu zija kwa akulu a ansembe ndi kwa akuluakulu.
4 Iye anati, "Ndachimwa pakuti ndapereka munthu wosalakwa."

Iwo anayankha nati, "Ife tilibe nazo kanthu izo ndi zako."

5 Pamenepo Yudasi anaponya ndalamazo m'Nyumba ya Mulungu
nachoka. Kenaka anapita nakadzimangirira.

6 Akulu a ansembe anatola ndalamazo nati, "Sikololedwa ndi lamulo
kuti ndalamazi tiziyike mosungira chuma cha Mulungu, popeza ndi
ndalama za magazi." 7 Choncho anagwirizana kuti ndalamazo azigwiritse
ntchito pogulira munda wa wowumba mbiya kuti ukhale manda alendo.
8 Ndi chifukwa chake umatchedwa munda wamagazi mpaka lero lino.
9 Pamenepo zimene anayankhula mneneri Yeremiya zinakwaniritsidwa
kuti, "Anatenga ndalama zamasiliva makumi atatu mtengo umene ana-
muyikira Iye anthu a Israeli. 10 Ndipo anazigwiritsa ntchito kugula munda
wa wowumba mbiya monga mmene Ambuye anandilamulira ine."

### *Yesu kwa Pilato*

11 Pa nthawi yomweyo Yesu anayimirira pamaso pa bwanamkubwa
ndipo bwanamkubwayo anamufunsa Iye kuti, "Kodi ndiwe Mfumu ya
Ayuda?"

Koma Yesu anayankha kuti, "Mwanena ndinu."

12 Pamene akulu a ansembe ndi akuluakulu ankamuneneza, sanayankhe
kanthu. 13 Kenaka Pilato anamufunsa Iye kuti, "Kodi sukumva zinthu
zimene akukuneneraz?" 14 Koma Yesu sanayankhe ngakhale mawu
amodzi mpaka bwanamkubwa anadabwa kwambiri.

15 Pa nthawiyi chinali chizolowezi cha bwanamkubwa kuti pachikondw-
erero cha Paska amamasula wam'ndende wosankhidwa ndi anthu. 16 Pa
nthawiyo anali ndi wam'ndende woyipa kwambiri dzina lake Baraba.
17 Gulu la anthu litasonkhana, Pilato anawafunsa kuti, "Ndi ndani amene
mufuna kuti ndikumasulireni; Baraba kapena Yesu wotchedwa Khristu?"
18 Pakuti anadziwa kuti anamupereka Yesu chifukwa cha kaduka.

19 Pamene Pilato anakhala pa mpando woweruza, mkazi wake anamu-
tumizira uthenga uwu, "Musachite kanthu ndi munthuyo, ndi wosalakwa
pakuti ndavutika kwambiri lero m'maloto chifukwa cha munthuyo."

20 Koma akulu a ansembe ndi akuluakulu ananyengerera gulu la anthu
kuti apemphe Baraba ndi kuti Yesu aphedwe.

21 Bwanamkubwayo anafunsa kuti, "Ndi ndani mwa awiriwa amene
mufuna ine ndikumasulireni?"

Iwo anayankha kuti, "Baraba."

22 Pilato anafunsa kuti, "Nanga ndichite chiyani ndi Yesu wotchedwa
Khristu?"

Onse anayankha kuti "Mpachikeni!"
23 Pilato anafunsa kuti, "Chifukwa chiyani? Wachita choyipa chotani?"
Koma anachita phokoso nafuwula kwambiri kuti, "Mpachikeni!"
24 Pilato ataona kuti samaphulapo kanthu, koma m'malo mwake chi-
wawa chimayambika, anatenga madzi nasamba m'manja mwake pamaso
pa gulu la anthu. Iye anati "Ine ndilibe chifukwa ndi magazi a munthu
uyu, ndipo uwu ndi udindo wanu!"
25 Anthu onse anayankha nati, "Magazi ake akhale pa ife ndi pa ana
athu!"
26 Pamenepo anawamasulira Baraba koma analamula kuti Yesu akak-
wapulidwe, ndipo anamupereka kuti akapachikidwe.

### *Asilikali Amuchita Chipongwe Yesu*

27 Pamenepo asilikali abwanamkubwayo anamutenga nalowa naye ku
bwalo la milandu ndipo anasonkhanitsa gulu lonse la asilikali namuzun-
gulira Iye. 28 Anamuvula malaya ake namuveka Iye malaya ofiira
aufumu. 29 Ndipo kenaka analuka chipewa chaminga nachiyika pa mutu
pake. Anamugwiritsa ndodo m'dzanja lake lamanja nagwada pamaso
pake namuchitira chipongwe nati, "Tikulonjereni Mfumu ya Ayuda."
30 Anamuthira malovu ndipo anatenga ndodo namumenya nayo pa mutu
mobwerezabwereza. 31 Atamaliza kumuchitira chipongwe, anamuvula
malaya aja namuveka malaya ake aja napita naye kokamupachika.

### *Amupachika Yesu*

32 Pamene guluILI linkatuluka ndi Yesu, anakumana ndi munthu wo-
chokera ku Kurene dzina lake Simoni ndipo anamuwumiriza kunyamula
mtanda. 33 Anafika ku malo wotchedwa Gologota amene atanthauza
kuti malo a bade la mutu. 34 Pamenepo anamupatsa vinyo wosakaniza
ndi ndulu kuti amwe; koma atalawa anakana kumwa. 35 Atamupachika
Iye, anagawana zovala zake pochita maere. 36 Ndipo anakhala pansi
namulonda Iye. 37 Pamwamba pa mutu wake analembapo mawu osonyeza
mlandu wake akuti, "UYU NDI YESU, MFUMU YA AYUDA." 38 Achifwamba
awiri anapachikidwa pamodzi ndi Iye, mmodzi kudzanja lamanja wina
kudzanja lamanzere. 39 Ndipo amene amadutsa anamunenera mawu a
chipongwe, akupukusa mitu yawo. 40 Ndipo anati, "Iwe amene ungapasule
Nyumba ya Mulungu ndi kuyimanga masiku atatu, dzipulumutse wekha!
Tsika pa mtandapo ngati ndiwe Mwana wa Mulungu!"
41 Chimodzimodzinso akulu a ansembe, aphunzitsi amalamulo ndi
akuluakulu anamuchitira chipongwe. 42 Iwo anati, "Anapulumutsa ena
koma sangathe kudzipulumutsa yekha! Ndi mfumu ya Israeli! Mulekeni
atsike pa mtanda ndipo tidzamukhulupirira Iye. 43 Amadalira Mulungu,
mulekeni Mulunguyo amupulumutse tsopano ngati akumufuna pakuti
anati, 'Ndine Mwana wa Mulungu.' " 44 Momwemonso mbala zimene
zinapachikidwa naye pamodzi zinamuneneranso zachipongwe.

### *Kufa kwa Yesu*

45 Kuyambira 12 koloko masana mpaka 3 koloko, kunachita mdima pa
dziko lonse. 46 Ndipo nthawi ili ngati 3 koloko, Yesu analira mofuwula
nati, "Eloi, Eloi, lama sabakitani!" Kutanthauza kuti, "Mulungu Wanga,
Mulungu Wanga, mwandisiyiranji Ine?"
47 Ena a oyimirira pamalopo atamva izi anati, "Akuyitana Eliya."

48 Mmodzi wa iwo anathamanga natenga chinkhupule. Anachidzaza
ndi vinyo wosasa, nachizika ku mtengo namupatsa Yesu kuti amwe.
49 Koma ena onse anati, “Mulekeni tiyeni tione ngati Eliyayo abwere
kudzamupulutsa.”
50 Ndipo pamene Yesu analiranso mofuwula, anapereka mzimu wake.
51 Pa nthawi imeneyo chinsalu chotchinga cha m’Nyumba ya Mulungu
chinang’ambika pakati kuyambira pamwamba mpaka pansi. Dziko
linagwedezeka ndipo miyala inang’ambika. 52 Manda anatsekuka ndipo
mitembo yambiri ya anthu oyera mtima amene anafa inaukitsidwa.
53 Anatuluka m’manda mwawo, ndipo chitachitika chiukitso cha Yesu,
anapita mu mzinda woyera naonekera kwa anthu ambiri.
54 Mkulu wa asilikali ndi amene ankalondera Yesu ataona chivomerezi
ndi zonse zinachitika, anachita mantha, ndipo anati, “Zoonadi, uyu anali
Mwana wa Mulungu!”
55 Amayi ambirimbiri amene ankasamalira Yesu ankaonerera ali patali.
Iwo anamutsatira Yesu kuchokera ku Galileya. 56 Pakati pawo panali
Mariya wa ku Magadala, Mariya amayi ake Yakobo ndi Yosefe ndi amayi
a ana a Zebedayo.

### *Yesu Ayikidwa M’manda*

57 Pamene kumada, kunabwera munthu wolemera wa ku Arimateyu
dzina lake Yosefe amene anali wophunzira wa Yesu. 58 Anapita kwa Pilato
kukapempha mtembo wa Yesu, ndipo Pilato analamula kuti uperekedwe
kwa iye. 59 Yosefe anatenga mtembowo, nawukulunga nsalu yabafuta.
60 Ndipo anawuyika m’manda ake atsopano amene anasema mu thanthwe,
natsekapo ndi mwala waukulu pa khomo la mandawo nachokapo.
61 Mariya wa Magadala ndi Mariya wina anakhala pansi moyang’anizana
ndi mandawo.

### *Alonda a pa Manda*

62 Litapita tsiku lokonzekera Sabata, mmawa mwake, akulu a ansembe
ndi Afarisi anapita kwa Pilato. 63 Iwo anati, “Bwana takumbukira kuti
munthu wonyenga uja akanali ndi moyo anati, ‘Pakatha masiku atatu
ndidzauka.’ 64 Choncho lamulirani kuti manda ake atetezedwe mpaka
pa tsiku lachitatu. Chifukwa tikapanda kutero, ophunzira ake angabwere
kudzaba mtembo wake ndipo angawuze anthu kuti waukitsidwa kwa
akufa. Ndipo chinyengo chomalizachi chidzakhala choyipa kwambiri
kusiyana ndi choyamba chija.”
65 Pilato anayankha kuti, “Tengani mlonda kalondereni monga mudzi-
wira.” 66 Tsono anapita nakatseka manda kolimba ndi kuyikapo
chizindikiro ndipo anayikapo mlonda.

## 28

### *Yesu Auka kwa Akufa*

1 Litapita tsiku la Sabata, mmawa wa tsiku loyamba la Sabata, Mariya
wa ku Magadala ndi Mariya wina anapita kukaona manda.
2 Kunachitika chivomerezi chachikulu, pakuti mngelo wa Ambuye
anabwera kuchokera kumwamba ndipo anapita ku manda, nakagubuduza
mwala nawukhalira. 3 Maonekedwe ake anali ngati mphenzi ndipo zovala
zake zinali mbuu ngati matalala. 4 Alondawo anachita naye mantha
kwambiri kotero kuti ananjenjemera ndi kuwuma ngati akufa.

5 Mngelo anati kwa amayiwo, “Musachite mantha popeza ndikudziwa
kuti mukufuna Yesu amene anapachikidwa. 6 Iye muno mulibe, wauka
monga mmene ananenera. Bwerani, dzaoneni malo amene anagona.
7 Ndipo pitani msanga kawuzeni ophunzira ake kuti, ‘Wauka kwa akufa
ndipo watsogola kupita ku Galileya. Mukamuona Iye kumeneko.’ Taonani
ndakuwuzani.”
8 Pamenepo amayiwo anachoka mofulumira ku mandako ali ndi man-
tha komabe atadzaza ndi chimwemwe, ndipo anathamanga kukawuza
ophunzira ake. 9 Mwadzidzidzi Yesu anakumana nawo nati, “Moni.” Iwo
anabwera kwa Iye, nagwira mapazi ake namulambira. 10 Ndipo Yesu
anawawuza kuti, “Musachite mantha, pitani kawuzeni abale anga kuti
apite ku Galileya ndipo kumeneko akandiona Ine.”

### *Uthenga wa Alonda*

11 Amayi aja akupita, ena mwa alonda aja anapita ku mzinda nafo-
tokozera akulu a ansembe zonse zimene zinachitika. 12 Akulu a ansembe
atakumana ndi akuluakulu anapangana zochita. Anapatsa alonda aja
ndalama zambiri, 13 nawawuza kuti, “Muzinena kuti, ‘Ophunzira ake
anabwera usiku ndipo amuba ife tili mtulo.’ 14 Ngati nkhani iyi imupeze
bwanamkubwa, ife tidzamukhazika mtima pansi ndipo simudzakhala
m’mavuto.” 15 Pamenepo alondawo anatenga ndalamazo nachita monga
mmene anawuzidwira. Ndipo mbiri iyi inawanda pakati pa Ayuda mpaka
lero lino.

### *Yesu Atuma Ophunzira Ake*

16 Ndipo ophunzira khumi ndi mmodzi aja anapita ku Galileya, ku phiri
limene Yesu anawawuza kuti apite. 17 Atamuona Iye, anamulambira;
koma ena anakayika. 18 Kenaka Yesu anabwera kwa iwo nati, “Ulamuliro
wonse kumwamba ndi dziko lapansi wapatsidwa kwa Ine. 19 Chifukwa
chake, pitani kaphunzitseni anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza
m’dzina la Atate ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera, 20 ndi kuwaphunzitsa
amvere zonse zimene ndinakulamulirani. Ndipo onani, Ine ndidzakhala
pamodzi ndi inu kufikira kutha kwa dziko lapansi pano.”

# UTHENGA WABWINO WA YESU KHRISTU WOLEMBEDWA NDI MARKO

### *Yohane M'batizi Akonza Njira*

1 Chiyambi cha Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu,
2 monga zalembedwera m'buku la mneneri Yesaya:
"Ine ndidzatuma mthenga wanga patsogolo panu,
amene adzakonza njira yanu,"
3 "Mawu a wofuwula m'chipululu,
'Konzani njira ya Ambuye,
wongolani njira zake.' "
4 Ndipo Yohane anabwera m'madera a m'chipululu nabatiza, ndi ku-
lalikira za ubatizo wa kutembenuka mtima ndi wa chikhululukiro cha
machimo. 5 Madera onse a ku Yudeya ndi anthu onse a ku Yerusalemu
anatuluka napita kwa iye. Akavomereza machimo awo, amawabatiza mu
mtsinje wa Yorodani. 6 Yohane amavala zovala zopangidwa ndi ubweya
wangamira, ndi lamba wachikopa m'chiwuno mwake, ndipo amadya
dzombe ndi uchi wamthengo. 7 Ndipo uthenga wake unali uwu: "Pambuyo
panga pakubwera wina wondiposa ine mphamvu. Ine si woyenera
kuwerama ndi kumasula zingwe za nsapato zake. 8 Ine ndikubatizani ndi
madzi, koma Iye adzakubatizani ndi Mzimu Woyera."

### *Kubatizidwa ndi Kuyesedwa kwa Yesu*

9 Pa nthawi imeneyo Yesu anabwera kuchokera ku Nazareti wa
ku Galileya ndipo anabatizidwa ndi Yohane mu mtsinje wa Yorodani.
10 Pamene Yesu ankatuluka m'madzi, anaona kumwamba kukutsekuka
ndipo Mzimu Woyera akutsikira pa Iye ngati nkhunda. 11 Ndipo
Mawu anamveka kuchokera kumwamba: "Iwe ndiwe Mwana wanga
wokondedwa; ndipo ndikondwera nawe."
12 Nthawi yomweyo Mzimu Woyera anamutumiza Iye ku chipululu,
13 ndipo anali m'chipululumo masiku makumi anayi, akuyesedwa ndi
Satana. Anali pakati pa nyama zakuthengo; ndipo angelo anamutumikira.

### *Yesu Alengeza za Uthenga Wabwino*

14 Yohane atamutsekera m'ndende, Yesu anapita ku Galileya nalalikira
Uthenga Wabwino wa Mulungu nati, 15 "Nthawi yafika, ufumu wa
Mulungu wayandikira. Tembenukani mtima ndi kukhulupirira Uthenga
Wabwino!"

### *Yesu Ayitana Ophunzira ake Oyamba*

16 Pamene Yesu ankayenda m'mbali mwa nyanja ya Galileya, anaona
Simoni ndi m'bale wake Andreya akuponya khoka m'nyanja, popeza anali
asodzi. 17 Yesu anati, "Bwerani, tsateni Ine, ndipo ndidzakusandutsani
asodzi a anthu." 18 Nthawi yomweyo anasiya makoka awo namutsata Iye.
19 Atapita patsogolo pang'ono, anaona Yakobo ndi m'bale wake Yohane
ana a Zebedayo, ali m'bwato akukonza makoka awo. 20 Mosataya nthawi
anawayitana, ndipo anasiya abambo awo Zebedayo ndi anyamata aganyu
ali m'bwatomo, namutsata Iye.

### *Yesu Atulutsa Mzimu Woyipa*

21 Iwo anapita ku Kaperenawo, ndipo tsiku la Sabata litafika, Yesu
analowa m'sunagoge nayamba kuphunzitsa. 22 Anthu anadabwa ndi
chiphunzitso chake, chifukwa anawaphunzitsa ngati munthu amene
anali ndi ulamuliro, osati ngati aphunzitsi amalamulo. 23 Pomwepo
munthu wina m'sunagogemo amene anali wogwidwa ndi mzimu woyipa
anafuwula kuti, 24 "Mukufuna chiyani kwa ife, Yesu wa ku Nazareti?
Kodi mwabwera kudzatiwononga? Ndikudziwa kuti ndinu ndani, ndinu
Woyerayo wa Mulungu!"

25 Yesu anadzudzula chiwandacho mwamphamvu nati, "Khala chete!
Tuluka mwa iye!" 26 Mzimu woyipawo unamugwedeza mwamphamvu
ndipo unatuluka mwa iye ukufuwula.

27 Anthu anadabwa kwambiri kotero kuti anafunsana wina ndi mnzake
kuti, "Ichi n'chiyani? Chiphunzitso chatsopano ndi ulamuliro! Iye aku-
lamula, ngakhale mizimu yoyipa ikumumvera." 28 Mbiri yake inafalikira
kudera lonse la Galileya mofulumira.

### *Yesu Achiritsa Anthu Ambiri*

29 Atangochoka mu sunagoge, Yesu pamodzi ndi Yakobo ndi Yohane
anakalowa m'nyumba ya Simoni ndi Andreya. 30 Mpongozi wa Simoni
anali chigonere akudwala malungo, ndipo anamuwuza Yesu za iye.
31 Ndipo Yesu anapita kwa iye, namugwira dzanja namuthandiza kudzuka.
Malungo anachoka ndipo anayamba kuwatumikira.

32 Madzulo omwewo dzuwa litalowa anthu anabweretsa kwa Yesu anthu
onse odwala ndi ogwidwa ndi ziwanda. 33 Anthu onse a m'mudzimo
anasonkhana pa khomo, 34 Yesu anachiritsa ambiri amene anali ndi
matenda osiyanasiyana, komanso anatulutsa ziwanda zambiri, ndipo
sanalole kuti ziwandazo ziyankhule chifukwa zinkamudziwa Iye.

### *Yesu Apemphera Kumalo a Yekha*

35 Mmamawa, kukanali kamdima, Yesu anadzuka, nachoka pa nyum-
bapo kupita kumalo kwa yekha, kumene anakapemphera. 36 Simoni ndi
anzake anapita kokamufunafuna Iye, 37 ndipo atamupeza, anamuwuza
kuti, "Aliyense akukufunani!"

38 Yesu anayakha kuti, "Tiyeni tipite kwina ku midzi ya pafupi kuti
ndikalalikirenso kumeneko. Ichi ndi chifukwa chimene ndinabwerera."
39 Potero anayendayenda mu Galileya, kulalikira m'masunagoge awo ndi
kutulutsa ziwanda.

### *Yesu Achiritsa Wakhate*

40 Munthu wakhate anabwera kwa Iye, nagwada, namupempha kuti,
"Ngati mukufuna, mukhoza kundiyeretsa."

41 Yesu pomva naye chifundo, anatambasula dzanja lake namukhudza
munthuyo nati, "Ndikufuna, yeretsedwa!" 42 Nthawi yomweyo khate
linachoka ndipo anachiritsidwa.

43 Nthawi yomweyo Yesu anamuwuza kuti apite koma anamuchenjeza
kuti, 44 "Wonetsetsa kuti usawuze aliyense za zimenezi. Koma pita,
kadzionetse wekha kwa wansembe ndi kukapereka nsembe zimene Mose
analamulira zotsimikizira kuyeretsedwa kwanu, ngati umboni kwa iwo."
45 M'malo mwake anapita nayamba kuyankhula momasuka, nafalitsa
mbiriyo. Zotsatira zake, Yesu sanathe kulowa m'mudzi moonekera, koma
anakhala kunja kumalo kopanda anthu. Komabe anthu amabwera kwa
Iye kuchokera kulikonse.

# 2

### *Yesu Achiritsa Munthu Wofa Ziwalo*

1 Patapita masiku pang'ono, Yesu atalowanso mu Kaperenawo, zi-
namveka kuti wabwera ali m'nyumba. 2 Choncho anthu ambiri ana-
sonkhana kotero kuti panalibenso malo, ngakhale ndi pa khomo pomwe,
ndipo Iye anawalalikira mawu. 3 Amuna anayi anabwera, atanyamula
munthu wofa ziwalo. 4 Popeza sakanatha kufika naye kwa Yesu chifukwa
cha gulu la anthu, anasasula denga chapamwamba pamene panali Yesu,
ndipo atabowoleza, anatsitsa mphasa yomwe munthu wofa ziwaloyo
anagonapo. 5 Yesu ataona chikhulupiriro chawo, anati kwa wofa ziwaloyo,
"Mwana, machimo ako akhululukidwa."
6 Ndipo ena mwa aphunzitsi amalamulo anakhala pansi pomwepo,
namaganiza m'mitima mwawo kuti, 7 "N'chifukwa chiyani munthuyu
ayankhula chotere? Iye akuchitira mwano Mulungu! Ndani angakhulu-
lukire munthu machimo kupatula Mulungu yekha?"
8 Nthawi yomweyo Yesu anadziwa mu mzimu wake kuti izi ndi zimene
ankaganiza m'mitima yawo, ndipo anawawuza kuti, "Chifukwa chiyani
mukuganiza zinthu izi? 9 Chapafupi n'chiyani; kunena kwa wofa ziwaloyu
kuti, 'Machimo ako akhululukidwa,' kapena kuti, 'Imirira, tenga mphasa
yako ndipo yenda?' 10 Koma kuti mudziwe kuti Mwana wa Munthu ali
ndi ulamuliro pa dziko lapansi wokhululukira machimo." Anati kwa
wofa ziwaloyo, 11 "Ndikuwuza iwe, imirira, tenga mphasa yako ndipo
pita kwanu." 12 Anayimirira, nanyamula mphasa yake natuluka onse
akumuona. Izi zinadabwitsa aliyense ndipo anayamika Mulungu nati,
"Sitinaonepo zinthu ngati izi!"

### *Kuyitanidwa kwa Levi*

13 Yesu anatulukanso napita kumbali ya nyanja. Gulu lalikulu la
anthu linabwera kwa Iye, ndipo anayamba kuliphunzitsa. 14 Pamene
ankayendabe, anaona Levi mwana wa Alufeyo atakhala m'nyumba ya
msonkho. Yesu anamuwuza kuti, "Tsate Ine." Ndipo Levi anayimirira
namutsata Iye.
15 Yesu atakalandira chakudya ku nyumba kwa Levi, amisonkho ambiri
ndi "ochimwa" ankadya naye pamodzi ndi ophunzira ake, pakuti anali
ambiri amene anamutsatira. 16 Pamene aphunzitsi amalamulo a Afarisi
anamuona akudya ndi "ochimwa" ndi amisonkho, anafunsa ophunzira
ake kuti, "Chifukwa chiyani amadya ndi olandira msonkho ndi ochimwa?"
17 Yesu atamva zimenezi, anawawuza kuti, "Anthu amene ali bwino
safuna sing'anga koma odwala. Ine sindinabwere kudzayitana olungama,
koma ochimwa."

### *Za Kusala Kudya*

18 Ndipo ophunzira a Yohane ndi a Afarisi amasala kudya. Anthu ena
anabwera kwa Yesu namufunsa kuti, "Zitheka bwanji kuti ophunzira a
Yohane ndi ophunzira a Afarisi amasala kudya, koma anu satero?"
19 Yesu anayankha nati, "Kodi alendo a mkwati angasale kudya bwanji
pamene iye ali nawo pamodzi? Iwo sangatero, pamene iye ali nawo
pamodzi. 20 Koma nthawi idzafika pamene mkwati adzachotsedwa pakati
pawo, ndipo pa tsiku limenelo adzasala kudya.
21 "Palibe amene amasokerera chigamba chatsopano pa chovala chakale.
Ngati atatero, chigamba chatsopanocho chidzazomola chovala chakalecho,

kukulitsa chibowocho. 22 Ndipo palibe amene amathira vinyo wat-
sopano m'matumba akale a vinyo. Ngati atatero, vinyo watsopanoyo
adzaphulitsa matumba a vinyo ndipo vinyoyo pamodzi ndi matumbawo
zidzawonongeka. Ayi, satero, amathira vinyo watsopano m'matumba
atsopanonso."

### *Yesu Mbuye wa Sabata*

23 Tsiku lina la Sabata, Yesu amadutsa pakati pa minda ya tirigu, ndipo
ophunzira ake amayenda naye limodzi, nayamba kubudula ngala za
tiriguyo. 24 Afarisi anati kwa Iye, "Taonani, chifukwa chiyani akuchita
chosaloledwa ndi lamulo pa Sabata?"

25 Iye anayankha kuti, "Kodi simunawerenge zimene Davide anachita
pamene iye ndi anzake anali osowa ndi anamva njala? 26 Pa nthawi ya
Abiatara mkulu wa ansembe, iye analowa m'nyumba ya Mulungu ndi
kudya buledi wopatulika amene amaloledwa kuti adye ndi ansembe okha.
Ndipo anapereka wina kwa anzake."

27 Pamenepo anawawuza kuti, "Sabata linapangidwira munthu, osati
munthu kupangidwira Sabata. 28 Choncho Mwana wa Munthu ali Ambuye
ngakhale wa Sabata."

# 3

### *Yesu Achiritsa Wolumala Dzanja*

1 Nthawi inanso analowa m'sunagoge, ndipo munthu wa dzanja
lolumala anali momwemo. 2 Ena a iwo anafunafuna chifukwa chakuti
akamuneneze Yesu, potero anamuyang'anitsitsa kuti aone ngati anga-
muchiritse tsiku la Sabata. 3 Yesu anati kwa munthu wolumala dzanjayo,
"Imirira, bwera kuno kutsogolo."

4 Ndipo Yesu anawafunsa kuti, "Kodi chololedwa ndi chiyani pa tsiku
la Sabata: kuchita chabwino kapena kuchita choyipa, kupulumutsa moyo
kapena kupha?" Koma iwo anakhala chete.

5 Yesu anawayang'ana ndi mkwiyo ndipo powawidwa mtima chifukwa
cha mitima yawo yowuma anati kwa munthuyo, "Wongola dzanja lako."
Iye analiwongola, ndipo dzanja lake linachira. 6 Kenaka Afarisi anatuluka
nayamba kukonza chiwembu ndi Aherode mmene angamuphere Yesu.

### *Magulu a Anthu Amutsata Yesu*

7 Yesu anachoka pamodzi ndi ophunzira ake napita ku nyanja, ndipo
gulu lalikulu la anthu lochokera ku Galileya linamutsata. 8 Atamva zonse
zimene amachita, anthu ambiri anabwera kwa Iye kuchokera ku Yudeya,
Yerusalemu, Idumeya ndi madera a ku tsidya kwa mtsinje wa Yorodani
ndi ozungulira Turo ndi Sidoni. 9 Chifukwa cha gulu la anthu, anawuza
ophunzira ake kuti apezeretu bwato likhale, kuti anthu angamupanikize.
10 Pakuti anachiritsa ambiri, kotero kuti iwo amene anali ndi matenda
amakankhana kutsogolo kuti amukhudze. 11 Nthawi iliyonse mizimu
yoyipa ikamuona, imagwa pansi pamaso pake ndi kufuwula kuti, "Inu
ndinu Mwana wa Mulungu!" 12 Koma anayichenjeza mwamphamvu kuti
isanene kuti Iye anali ndani.

### *Yesu Asankha Ophunzira Khumi ndi Awiri*

13 Yesu anakwera ku phiri ndipo anayitana amene anawafuna, ndipo
anabwera kwa Iye. 14 Iye anasankha khumi ndi awiri, nawayika akhale
atumwi; pokhala ndi Iye aziwatuma kukalalikira 15 ndi kuti akhale

ndi ulamuliro wotulutsa ziwanda. 16 Awa ndi khumi ndi awiri amene
anawasankha: Simoni (amene anapatsidwa dzina lakuti Petro); 17 Yakobo
mwana wa Zebedayo, ndi m'bale wake Yohane (iwowa anawapatsa dzina
lakuti Bowanege, ndiye kuti ana a bingu); 18 Andreya, Filipo, Bartumeyu,
Mateyu, Tomasi, Yakobo mwana wa Alufeyo, Tadeyo, Simoni Zelote, 19 ndi
Yudasi Isikarioti, amene anamupereka Iye.

### *Yesu ndi Belezebabu*

20 Pambuyo pake Yesu analowa m'nyumba, ndipo gulu la anthu
linasonkhananso, kotero kuti Iye pamodzi ndi ophunzira ake sanapeze
mpata kuti adye. 21 Anthu a ku banja lake atamva zimenezi, anapita kuti
akamutenga, pakuti ankanena kuti, "Wazungulira mutu."

22 Ndipo aphunzitsi amalamulo omwe anachokera ku Yerusalemu anati,
"Iye wagwidwa ndi Belezebabu! Ndi ulamuliro wa mkulu wa ziwanda
akutulutsa ziwanda."

23 Pamenepo Yesu anawayitana nawayankhula m'mafanizo nati: "Kodi
Satana angatulutse bwanji Satana? 24 Ngati ufumu ugawanikana mwa
iwo okha, ufumu umenewo sungakhalitse. 25 Ngati nyumba igawanikana
mwa iyo yokha, nyumba imeneyo singathe kuyima. 26 Ndipo ngati Satana
adzitsutsa yekha sangathe kuyima; ulamuliro wake watha. 27 Kunena
zoona, palibe munthu angalowe m'nyumba ya munthu wamphamvu
ndi kutenga katundu wake pokhapokha atayamba wamumanga munthu
wamphamvuyo. Pamenepo akhoza kumubera. 28 Ndikukuwuzani zoona
kuti machimo onse ndi zamwano zonse za anthu zidzakhululukidwa,
29 koma aliyense amene achitira mwano Mzimu Woyera sadzakhulu-
lukidwa pakuti wachita tchimo losatha."

30 Ananena izi chifukwa anati, "Ali ndi mzimu woyipa."

### *Amayi ndi Abale ake a Yesu*

31 Pamenepo amayi ndi abale ake a Yesu anafika. Atayima kunja,
anatuma wina kuti akamuyitane Iye. 32 Gulu la anthu linakhala mo-
muzungulira Iye, ndipo anamuwuza kuti, "Amayi ndi abale anu ali panja
akukufunani."

33 Iye anafunsa kuti, "Amayi ndi abale anga ndi ndani?"

34 Pamenepo anayang'ana anthu amene anakhala momuzungurira
ndipo anati, "Awa ndi amayi anga ndi abale anga! 35 Aliyense amene
achita chifuniro cha Mulungu ndi m'bale wanga ndi mlongo wanga ndi
amayi anga."

## 4

### *Fanizo la Wofesa Mbewu*

1 Nthawi inanso Yesu atakhala m'mbali mwa nyanja, anayamba ku-
phunzitsa. Gulu lalikulu la anthu linasonkhana momuzungulira kotero
kuti Iye analowa m'bwato lomwe linali pa nyanja nakhalamo, anthu onse
ali pa mtunda m'mbali mwa madzi. 2 Anawaphunzitsa zinthu zambiri
m'mafanizo, ndipo m'chiphunzitso chake anati: 3 "Tamverani! Mlimi
anapita kukafesa mbewu zake. 4 Akufesa, mbewu zina zinagwera m'mbali
mwa njira, ndipo mbalame zinabwera ndi kuzidya. 5 Zina zinagwa pa
malo a miyala pamene panalibe dothi lambiri. Zinamera mofulumira
chifukwa panalibe dothi lambiri. 6 Koma dzuwa litakwera, mbewuzo
zinapserera, ndipo zinawuma chifukwa zinalibe mizu. 7 Mbewu zina

zinagwa pa minga, ndipo mingayo inayanga ndi kuzirepheretsa kukula.
8 Mbewu zinanso zinagwa pa nthaka yabwino ndipo zinamera, zinakula
ndi kubereka zipatso, zina zochuluka makumi atatu, zina makumi asanu
ndi limodzi ndi zina 100."
9 Pamenepo Yesu anati, "Amene ali ndi makutu akumva, amve."
10 Ali yekha, ophunzira ndi ena omuzungulira, anamufunsa za mafanizo.
11 Iye anawawuza kuti, "Chinsinsi cha ufumu wa Mulungu chapatsidwa
kwa inu. Koma kwa amene ali kunja zinthu zonse zinenedwa m'mafanizo:
12 kotero kuti,
" 'Kupenya mudzapenya koma osaona kanthu,
kumva mudzamva koma osamvetsetsa,
kuti mwina angatembenuke ndi kukhululukidwa!' "
13 Pamenepo Yesu anawawuza kuti, "Kodi simukulimvetsa fanizoli? Kodi
nanga mudzazindikira bwanji fanizo lina lililonse? 14 Wofesa amafesa
mawu. 15 Anthu ena ali ngati mbewu za m'mbali mwa njira, m'mene
mawu amafesedwamo. Akangowamva, Satana amabwera ndi kuchotsa
mawu amene anafesedwa mwa iwo. 16 Ena, monga mbewu zofesedwa
pa miyala, amamva mawu ndipo nthawi yomweyo amawalandira ndi
chimwemwe. 17 Koma popeza alibe mizu, amakhala kwa kanthawi
kochepa. Mavuto kapena masautso akafika chifukwa cha mawu, amagwa
mofulumira. 18 Komabe ena, monga mbewu zofesedwa pakati pa minga,
amamva mawu; 19 koma nkhawa zamoyo uno, chinyengo cha chuma
ndi zokhumba za zinthu zina zimabwera ndi kutchinga mawu, ndipo
amawachititsa kukhala osabala chipatso. 20 Ena, ngati mbewu zofesedwa
pa nthaka yabwino, amamva mawu, nawalandira, ndi kubereka zipatso
zokwanira makumi atatu, makumi asanu ndi limodzi, kapena ngakhale
100 kuwonjezera pa zomwe zinafesedwa."

### *Fanizo la Nyale*

21 Iye anawawuza kuti, "Kodi umatenga nyale ndi kuyiika pansi pa
mbiya kapena pansi pa bedi? M'malo mwake, kodi simuyika pa choyikapo
chake? 22 Pakuti chilichonse chobisika chidzayenera kuwululika, ndi
chilichonse chachinsinsi chidzayenera kuonekera poyera. 23 Ngati wina
ali ndi makutu akumva, amve."
24 Anapitiriza nati, "Ganizirani mosamala zimene mukumva, ndi
muyeso umene mugwiritsa ntchito, mudzayesedwa nawo, ndipo ngakhale
kwambiri. 25 Amene ali nazo adzapatsidwa zochuluka; amene alibe,
ngakhale zimene ali nazo zidzachotsedwa kwa iwo."

### *Fanizo la Mbewu Imene Ikukula*

26 Iye anatinso, "Umu ndi mmene ulili ufumu wa Mulungu. Munthu
amafesa mbewu m'nthaka. 27 Usiku ndi usana, kaya agona kapena adzuka,
mbewu imamera ndi kukula, ngakhale sadziwa mmene zimachitikira.
28 Nthaka pa yokha imatulutsa mbewu, umayamba m'mera, kenaka
ngala, kenaka mbewu yokhwima m'ngalayo. 29 Mbewuyo ikangokhwima,
amayimweta chifukwa nthawi yokolola yakwana."

### *Fanizo la Mbewu ya Mpiru*

30 Ndipo anatinso, "Kodi tinene kuti ufumu wa Mulungu ufanana ndi
chiyani, kapena ndi fanizo lotani limene tidzagwiritsa ntchito pakuwu-
fotokozera? 31 Uli ngati mbewu ya mpiru imene ndi mbewu yaying'ono
kwambiri yomwe mumadzala m'nthaka. 32 Koma ikadzalidwa, imakula

ndi kukhala yayikulu koposa mbewu zina zonse za m'munda ndipo
m'nthambi zake zazikulu mbalame zamlengalenga zimadzapuma pa
mthunzi wake."
33 Ndi mafanizo ambiri onga awa Yesu anayankhula mawu kwa
iwo, monga mmene akanatha kumvetsa. 34 Iye sananene kanthu kwa
iwo osagwiritsa ntchito fanizo. Koma ali yekha ndi ophunzira ake,
ankawatanthauzira zonse.

### *Yesu Aletsa Namondwe*

35 Tsiku limenelo atafika madzulo, anawuza ophunzira ake kuti, "Tiyeni
tiwolokere tsidya lina." 36 Atasiya gulu la anthu m'mbuyo, anamutenga
Iye, napita naye monga momwe anali m'bwatolo. Panalinso mabwato
ena pamodzi ndi Iye. 37 Mphepo yamkuntho inabuka, ndipo mafunde
anawomba bwatolo, kotero kuti linali pafupi kumira. 38 Pa nthawi imeneyi
Yesu anali akugona atatsamira pilo kumbuyo kwa bwato. Ophunzira
anamudzutsa nati kwa Iye, "Aphunzitsi, kodi simukusamala kuti timira?"
39 Yesu anauka nadzudzula mphepo nati kwa mafunde, "Chete! Khala
bata!" Pamenepo mphepo inaleka ndipo kunachita bata.
40 Iye anati kwa ophunzira ake, "Muli ndi mantha chifukwa chiyani?
Kodi mukanalibe chikhulupiriro?"
41 Iwo anachita mantha nafunsana wina ndi mnzake kuti, "Uyu ndani?
Ngakhale mphepo ndi nyanja zimumvera Iye!"

## 5

### *Yesu Achiritsa Wogwidwa ndi Ziwanda*

1 Ndipo anawoloka nyanja napita ku dera la Gerasa. 2 Yesu atatuluka
m'bwato, munthu amene anali ndi mzimu woyipa anachoka ku manda ndi
kukumana naye. 3 Munthuyu amakhala ku manda, ndipo panalibe amene
akanatha kumumanganso ngakhale ndi unyolo. 4 Pakuti nthawi zambiri
akamumanga manja ndi miyendo amadula maunyolo ndi kudula zitsulo
zimene zinali m'mapazi ake. Panalibe amene anali ndi mphamvu yoti
ndi kumugonjetsa. 5 Usana ndi usiku ankakhala ku manda ndi kumapiri,
akulira ndi kudzicheka ndi miyala.
6 Ataona Yesu ali patali, anathamanga nagwa pa mawondo ake pamaso
pake. 7 Iye anafuwula kwambiri nati, "Mukufuna muchite nane chiyani,
Yesu Mwana wa Mulungu Wammwambamwamba? Lumbirani kwa
Mulungu kuti simundizunza!" 8 Pakuti Yesu anati kwa iye, "Tuluka mwa
munthuyu, iwe mzimu woyipa!"
9 Ndipo Yesu anamufunsa iye, "Dzina lako ndani?"
Iye anayankha kuti, "Dzina langa ndine Legiyo, pakuti tilipo am-
biri." 10 Ndipo anamupempha Yesu mobwerezabwereza kuti asazitulutse
m'deralo.
11 Gulu lalikulu la nkhumba limadya m'mbali mwa phiri limene linali
pafupi. 12 Ziwandazo zinapempha Yesu kuti, "Titumizeni pakati pa
nkhumbazo; ndipo mutilole tilowe mwa izo." 13 Iye anazipatsa chilolezo,
ndipo mizimu yoyipayo inatuluka ndi kukalowa mu nkhumbazo. Gulu
la nkhumba, zokwana pafupifupi 2,000 zinathamanga kutsetserekera ku
nyanja ndipo zinamira.
14 Omwe amaweta nkhumbazo anathawa ndi kukawuza anthu za izi mu
mzinda ndi ku madera a ku midzi, ndipo anthu anapita kukaona zomwe
zinachitika. 15 Atafika kwa Yesu, anaona munthu amene anagwidwa

ndi ziwanda zambiri uja atakhala pansi pomwepo, atavala, ndipo ali
bwinobwino. Iwo anachita mantha. 16 Amene anaona zimenezi anawuza
anthu zomwe zinachitika kwa munthu wogwidwa ndi ziwandayo ndipo
anawawuzanso za nkhumbazo. 17 Ndipo anthu anayamba kumupempha
Yesu kuti achoke m'dera lawo.

18 Yesu akulowa m'bwato, munthu amene anagwidwa ndi ziwanda uja
anamupempha kuti apite nawo. 19 Yesu sanamulole, koma anati, "Pita
kwanu ku banja lako ndipo ukawawuze zimene Ambuye wakuchitira, ndi
chifundo chimene wakuchitira." 20 Pomwepo munthuyo anapita nayamba
kuwuza anthu a ku Dekapoli zinthu zimene Yesu anamuchitira. Ndipo
anthu onse anadabwa.

### *Mtsikana Womwalira ndi Mayi Wodwala*

21 Yesu atawolokeranso pa bwato kupita mbali ina ya nyanja, gulu
lalikulu la anthu linasonkhana momuzungulira. Ali m'mbali mwa nyanja,
22 mmodzi wa akulu a m'sunagoge, dzina lake Yairo anafika pamenepo.
Ataona Yesu, anagwa pa mapazi ake, 23 ndi kumudandaulira kwambiri
nati, "Mwana wanga wamkazi wamng'ono ali pafupi kufa. Chonde
tiyeni kuti mukamusanjike manja kuti akachiritsidwe nakhala ndi moyo."
24 Ndipo Yesu anapita naye.

Gulu lalikulu la anthu linamutsata ndi kumamupanikiza Iye.
25 Pomwepo panali mayi amene amadwala nthenda yotaya magazi kwa
zaka khumi ndi ziwiri. 26 Iye anavutika kwambiri pamene asing'anga
ambiri ankamusamalira ndipo anagwiritsa ntchito zonse anali nazo,
koma m'malo mochira, nthenda yake inkakulakulabe. 27 Atamva za Yesu,
anabwera kumbuyo kwake m'gulu la anthu ndipo anakhudza mkanjo
wake, 28 chifukwa anaganiza kuti, "Ngati nditangokhudza mkanjo wake,
ndidzachiritsidwa." 29 Nthawi yomweyo magazi ake analeka kutuluka
ndipo anamva m'thupi mwake kuti wamasulidwa ku vuto lake.

30 Pomwepo Yesu anazindikira kuti mphamvu inachoka m'thupi mwake.
Anatembenuka m'gulu la anthu ndipo anafunsa kuti, "Ndani wakhudza
zovala zanga?"

31 Ophunzira ake anayankha kuti, "Mukuona kuti anthu akuku-
panikizani, ndipo Inu mukufunsa kuti, 'Ndani wandikhudza?' "

32 Koma Yesu anapitirizabe kuyang'ana kuti aone amene anachita
zimenezi. 33 Kenaka mayi uja pozindikira chimene chinamuchitikira,
anabwera ndi kugwa pa mapazi ake, ndipo akunjenjemera ndi mantha,
anamuwuza zoona zokhazokha. 34 Anati kwa iye, "Mwana wamkazi,
chikhulupiriro chako chakuchiritsa. Pita mu mtendere ndipo khala
womasulidwa ku mavuto ako."

35 Pamene Yesu ankayankhulabe, amuna ena anafika kuchokera ku
nyumba ya Yairo, mkulu wa sunagoge. Iwo anati, "Mwana wanu wamkazi
wamwalira, muvutitsiranjinso aphunzitsiwa?"

36 Posasamala zomwe ananena, Yesu anamuwuza mkulu wa sunagoge
uja kuti, "Usachite mantha; ingokhulupirira."

37 Iye sanalole munthu wina aliyense kuti amutsatire koma Petro,
Yakobo ndi Yohane m'bale wa Yakobo. 38 Atafika ku nyumba ya mkulu
wa sunagoge, Yesu anaona chipiringu cha anthu akulira ndi kufuwula
kwambiri. 39 Analowa nati kwa iwo, "Mukuchita phokoso ndi kulira
chifukwa chiyani? Mwanayu sanamwalire koma ali mtulo." 40 Koma
anamuseka Iye.

Atawatulutsa onse panja, Iye anatenga abambo ndi amayi ake a
mwanayo ndi ophunzira omwe anali naye, ndipo analowa m'mene munali
mwanayo. 41 Anagwira dzanja lake nanena kwa iye, "Talita Kumi!"
(Kutanthauza kuti, "Mtsikana, ndikunena ndi iwe, imirira!") 42 Nthawi
yomweyo anayimirira nayenda mozungulira (anali wa zaka khumi ndi
ziwiri). Pa ichi onse anadabwa kwambiri. 43 Anawalamulira kwambiri
kuti asawuze wina aliyense za ichi, ndipo anawawuza kuti amupatse
kanthu koti adye.

# 6

### *Amupeputsa Yesu ku Nazareti*

1 Yesu anachoka kumeneko napita ku mudzi kwawo, pamodzi ndi
ophunzira ake. 2 Tsiku la Sabata litafika, anayamba kuphunzitsa
m'sunagoge, ndipo ambiri amene anamumva anadabwa.

Iwo anafunsa kuti, "Kodi munthu uyu anazitenga kuti zimenezi?
Kodi ndi nzeru yotani imene munthu ameneyu wapatsidwa, kuti Iye
akuchitanso zodabwitsa! 3 Kodi uyu si mpalamatabwa uja? Kodi uyu si
mwana wa Mariya ndi m'bale wa Yakobo, Yose, Yudasi ndi Simoni? Kodi
alongo ake si ali ndi ife?" Ndipo anakhumudwa naye.

4 Yesu anawawuza kuti, "Mneneri amalemekezedwa kulikonse kupatula
kwawo, ndi pakati pa abale ake ndi a m'banja mwake." 5 Sanachite
zodabwitsa kumeneko, koma anangosanjika manja pa odwala ochepa ndi
kuwachiritsa. 6 Ndipo Iye anadabwa chifukwa chakusowa chikhulupiriro
kwawo.

### *Yesu Atuma Ophunzira Khumi ndi Awiri*

Pamenepo Yesu anayenda mudzi ndi mudzi kuphunzitsa. 7 Atayitana
khumi ndi awiriwo, Iye anawatuma awiriawiri ndipo anawapatsa ula-
muliro pa mizimu yoyipa.

8 Zomwe anawalangiza ndi izi: "Musatenge kanthu ka paulendo koma
ndodo yokha; osatenga buledi, thumba, kapena ndalama. 9 Muvale
nsapato koma osatenga malaya apadera. 10 Pamene mulowa m'nyumba
mukakhale momwemo kufikira mutachoka m'mudzimo. 11 Ndipo ngati pa
malo ena sakakulandirani kapena kukumverani, sasani fumbi la kumapazi
anu pamene mukuchoka, kuti ukhale umboni wowatsutsa."

12 Anatuluka kupita kukalalikira kuti anthu atembenuke mtima.
13 Anatulutsa ziwanda zambiri ndi kudzoza mafuta odwala ambiri ndi
kuwachiritsa.

### *Yohane M'batizi Adulidwa Mutu*

14 Mfumu Herode anamva zimenezi, pakuti dzina la Yesu linali litadzi-
wika kwambiri. Ena amati, "Yohane M'batizi waukitsidwa kwa akufa,
ndipo n'chifukwa chake mphamvu zochita zodabwitsa zinkagwira ntchito
mwa Iye."

15 Ena anati, "Iye ndi Eliya."

Enanso anati, "Ndi mneneri, ofanana ndi mmodzi wa aneneri akale."

16 Koma Herode atamva zimenezi anati, "Yohane, munthu amene
ndinamudula mutu, waukitsidwa kuchokera kwa akufa."

17 Pakuti Herode iye mwini analamula kuti amumange Yohane ndi
kumuyika m'ndende. Anachita izi chifukwa cha Herodia, mkazi wa m'bale
wake Filipo, amene iye anamukwatira. 18 Pakuti Yohane ankanena kwa
Herode kuti, "Sikololedwa kwa inu kuti mukwatire mkazi wa m'bale

wanu.” 19 Ndipo Herodia anamusungira Yohane chidani ndipo anafuna
kumupha, koma sanathe kutero, 20 chifukwa Herode anaopa Yohane
ndipo anamuteteza, podziwa kuti iye anali munthu wolungama ndi
woyera mtima. Herode akamamva Yohane, ankathedwa nzeru; komabe
amakonda kumumvetsera.
21 Pomaliza mpata unapezeka. Pa tsiku lokumbukira kubadwa kwake,
Herode anakonzera phwando akuluakulu ake, akulu a ankhondo ndi
anthu odziwika a mu Galileya. 22 Mwana wamkazi wa Herodia atabwera
ndi kudzavina, anakondweretsa Herode ndi alendo ake a pa mphwandopo.

Mfumu inati kwa mtsikanayo, “Undipemphe chilichonse chimene
ukuchifuna, ndipo ndidzakupatsa.” 23 Ndipo analonjeza ndi lumbiriro
kuti, “Chilichonse chimene upempha ndidzakupatsa, ngakhale theka la
ufumu wanga.”

24 Iye anatuluka nati kwa amayi ake, “Kodi ndikapemphe chiyani?”

Iye anamuyankha kuti, “Mutu wa Yohane M’batizi.”

25 Nthawi yomweyo mtsikana uja anafulumira kupita komwe kunali
mfumu ndi pempho lake: “Ndikufuna kuti mundipatse pomwe pano mutu
wa Yohane M’batizi m’mbale.”

26 Mfumu inamva chisoni chachikulu, koma chifukwa cha lumbiro lake
ndi alendo ake a pa mphwandolo, sanafune kumukaniza. 27 Nthawi
yomweyo iye anatumiza yemwe anali ndi ulamuliro wonyonga anthu
kuti abweretse mutu wa Yohane. Munthuyo anapita, nakadula mutu
wa Yohane m’ndende, 28 nabweretsa mutuwo m’mbale. Anawupereka
kwa mtsikanayo, ndipo iye anakapereka kwa amayi ake. 29 Atamva
izi, ophunzira a Yohane anabwera nadzatenga mtembo ndi kukawuyika
m’manda.

### *Yesu Adyetsa Anthu 5,000*

30 Atumwi anasonkhana mozungulira Yesu namufotokozera zonse
zomwe anachita ndi kuphunzitsa. 31 Popeza kuti panali anthu ambiri
amene amabwera ndi kumapita, analibe mpata wakuti adye, ndipo Iye
anawawuza kuti, “Tiyeni kuno kumalo achete kuti tikapume.”

32 Ndipo anachoka okha pa bwato napita kumalo a okhaokha. 33 Koma
ambiri amene anawaona akuchoka anawazindikira ndipo anathamanga
wapansi kuchokera m’midzi yonse nakayambirira kufika. 34 Yesu atafika
ku mtunda ndi kuona gulu lalikulu la anthu, anamva nawo chisoni
chifukwa anali ngati nkhosa zopanda m’busa. Ndipo anayamba kuwa-
phunzitsa zinthu zambiri.

35 Pa nthawi iyi n’kuti dzuwa litapendeka, ndipo ophunzira ake anabw-
era kwa Iye nati, “Kuno ndi kuthengo, ndipo ano ndi madzulo. 36 Awuzeni
anthuwa azipita ku midzi ndi madera ozungulira, kuti akadzigulire kanthu
kakuti adye.”

37 Koma Iye anayankha kuti, “Apatseni kanthu koti adye.”

Iwo anati kwa Iye, “Apa pafunika ndalama za miyezi isanu ndi itatu
zomwe munthu amalandira! Kodi tipite kukagwiritsa ntchito ndalama
zotere kugulira buledi kuti tiwapatse adye?”

38 Iye anawafunsa kuti, “Muli ndi malofu a buledi angati? Pitani
mukaone.”

Ataona anati kwa Iye, “Asanu ndi nsomba ziwiri.”

39 Pamenepo Yesu anawalamulira kuti awakhazike anthu pansi
m’magulu pa msipu obiriwira. 40 Ndipo anakhala pansi m’magulu a
anthu 100 ndi gulu la anthu makumi asanu. 41 Atatenga malofu a

buledi asanu ndi nsomba ziwiri, nayang'ana kumwamba, Iye anayamika
nagawa malofu a bulediwo. Kenaka anawapatsa ophunzira ake kuti
awapatse anthu. Ndipo anagawanso nsomba ziwirizo kwa onse. 42 Onse
anadya ndipo anakhuta, 43 ndipo ophunzira ake anatola buledi ndi nsomba
zotsalira zokwanira madengu khumi ndi awiri. 44 Chiwerengero cha
amuna amene anadya chinali 5,000.

### *Yesu Ayenda pa Nyanja*

45 Nthawi yomweyo Yesu anawuza ophunzira ake kuti alowe m'bwato
ndi kuti atsogole kupita ku Betisaida, pamene Iye ankawuza anthu kuti
azipita. 46 Atawasiya, Iye anakwera ku phiri kukapemphera.

47 Pofika madzulo, bwato linali pakati pa nyanja, ndipo Iye anali
yekha pa mtunda. 48 Iye anaona ophunzira ake akuvutika popalasa
bwato, chifukwa mphepo imawomba mokumana nawo. Pa nthawi ya
m'bandakucha Iye anafika kwa iwo akuyenda pa nyanja. Anali pafupi
kuwapitirira, 49 koma atamuona Iye akuyenda pa nyanja, anaganiza kuti
anali mzukwa. Iwo anafuwula, 50 pakuti onse anamuona ndipo anachita
mantha.

Nthawi yomweyo Iye anawayankhula nati, "Limbani mtima! Ndine.
Musachite mantha." 51 Ndipo Iye anakwera m'bwato pamodzi nawo,
ndipo mphepo inaleka. Iwo anadabwa kwambiri, 52 popeza sanazindikire
zimene zinachitika pa malofu a buledi; pakuti mitima yawo inali yowuma.

53 Atawoloka, anafika ku Genesareti nayima pa dooko. 54 Atangotuluka
m'bwato, anthu anamuzindikira Yesu. 55 Anathamanga uku ndi uko
m'dera lonse nakanyamula odwala pa machira kupita nawo kulikonse
kumene anamva kuti kuli Iye. 56 Ndipo kulikonse kumene anapita, ku
midzi, m'mizinda ndi madera a ku midzi, iwo anayika odwala m'malo
a m'misika. Iwo anamupempha kuti awalole kuti akhudze ngakhale
mphonje za mkanjo wake, ndipo onse amene anamukhudza anachira.

## 7

### *Miyambo ya Makolo ya Ayuda*

1 Afarisi ndi ena mwa aphunzitsi amalamulo omwe anachokera ku
Yerusalemu anasonkhana momuzungulira Yesu ndipo 2 iwo anaona
ophunzira ake akudya chakudya ndi m'manja mwakuda kapena kuti
m'manja mosasamba. 3 (Afarisi ndi Ayuda onse sadya pokhapokha
atasamba m'manja, kusunga mwambo wa makolo awo. 4 Akabwera
kuchokera ku msika samadya pokhapokha atasamba. Ndipo amasunga
miyambo ina yambiri monga, kutsuka zikho, mitsuko ndi maketulo).

5 Choncho Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo anafunsa Yesu kuti,
"N'chifukwa chiyani ophunzira anu satsatira mwambo wa makolo,
m'malo mwake amangodya chakudya ndi m'manja mwakuda?"

6 Iye anayankha kuti, "Yesaya ananena zoona pamene ananenera za inu
achiphamaso; monga kunalembedwa kuti:

"Anthu awa amandilemekeza Ine ndi milomo yawo,
koma mitima yawo ili kutali ndi Ine.
7 Amandilambira Ine kwachabe;
ndi kuphunzitsa malamulo ndi malangizo a anthu.
8 Mwasiya malamulo a Mulungu ndipo mwagwiritsitsa miyambo ya
anthu."

9 Ndipo anawawuzanso kuti, “Inu muli ndi njira yabwino yokankhira
kumbali malamulo a Mulungu kuti mukatsatire miyambo yanuyo!
10 Pakuti Mose anati, ‘Lemekeza abambo ako ndi amayi ako,’ ndipo,
‘aliyense amene atemberera abambo ake kapena amayi ake ayenera
kuphedwa.’ 11 Koma inu mumati, ngati munthu anena kwa abambo
ake kapena amayi ake kuti, ‘Thandizo lililonse mukanayenera kulandira
kuchokera kwa ine ndi Korobani’ (kutanthauza kuti, mphatso yop-
erekedwa kwa Mulungu), 12 pamenepo inu simumalola kuti achitire
kanthu kalikonse abambo kapena amayi ake. 13 Potero mumachepetsa
mawu a Mulungu kukhala wopanda mphamvu ndi miyambo yanu imene
mumapatsirana. Ndipo mumachita zinthu zina zambiri monga zimenezi.”
14 Yesu anayitananso gulu la anthu ndipo anati, “Tandimverani nonsenu,
ndipo zindikirani izi. 15 Palibe kanthu kunja kwa munthu kamene
kakalowa mwa iye kangamusandutse wodetsedwa. Koma zimene zituluka
mwa munthu ndizo zimupanga kukhala wodetsedwa.” 16 (Ngati wina ali
ndi makutu akumva amve).
17 Atalisiya gulu la anthu ndi kulowa m’nyumba, ophunzira ake anamu-
funsa za fanizoli 18 Iye anawafunsa kuti, “Kodi nanunso simumvetsetsa?
Kodi simukuona kuti palibe kanthu kamene kakalowa mwa munthu
kochokera kunja kakhoza kumudetsa? 19 Pakuti sikalowa mu mtima wake
koma m’mimba mwake, ndipo kenaka kamatuluka kunja.” (Ndi mawu
amenewa, Yesu anayeretsa zakudya zonse).
20 Anapitiriza kuti, “Chimene chichokera mwa munthu ndi chomwe
chimamudetsa. 21 Pakuti kuchokera m’kati mwa mitima ya anthu,
mumatuluka maganizo oyipa, chiwerewere, kuba, kupha, chigololo,
22 dyera, nkhwidzi, chinyengo, machitidwe onyansa, kaduka, chipongwe,
kudzikuza ndi kupusa. 23 Zoyipa zonsezi zimatuluka m’kati ndipo
zimadetsa munthu.”

### *Chikhulupiriro cha Mayi wa ku Siriya Fonisia*

24 Yesu anachoka kumalo amenewo napita ku madera a Turo. Iye
analowa m’nyumba ndipo sanafune wina kuti adziwe zimenezi; komabe
sanathe kudzibisa. 25 Kunena zoona, amayi amene kamwana kawo
kakakazi kanali kogwidwa ndi mzimu woyipa, atangomva za Iye, anab-
wera nagwada pa mapazi ake. 26 Mayiyu anali Mhelene, wobadwira ku
Fonisia wa ku Siriya. Anamupempha Yesu kuti atulutse chiwanda mwa
mwana wake.
27 Iye anamuwuza kuti, “Choyamba asiye ana adye zimene akuzifuna,
pakuti si kwabwino kutenga buledi wa ana ndi kuponyera agalu awo.”
28 Mayiyo anayankha kuti, “Inde Ambuye, koma ngakhale agalu amadya
zomwe zimagwa pansi kuchokera pa tebulo la ana.”
29 Ndipo Iye anamuwuza kuti, “Chifukwa cha yankholi, ukhoza kupita;
chiwanda chachoka mwa mwana wako wamkazi.”
30 Atapita kwawo anakapeza mwana wake aligone pa bedi, chiwanda
chitatuluka.

### *Kuchiritsidwa kwa Munthu Wosamva ndi Wosayankhula*

31 Ndipo Yesu anachoka ku dera la Turo nadutsa pakati pa Sidoni,
kutsikira ku nyanja ya Galileya kupita ku dera la Dekapoli. 32 Kumeneko
anthu ena anabweretsa kwa Iye munthu amene anali wosamva ndi
wosayankhula, ndipo anamupempha kuti asanjike dzanja pa iye.
33 Atamutengera iye pambali, patali ndi gulu la anthu, Yesu analowetsa
zala zake m’makutu a munthuyo. Kenaka anapaka malovu pachala ndi

kukhudza lilime la munthuyo. 34 Iye anayang'ana kumwamba ndipo
ndi mawu otsitsa moyo, anati kwa iye, "Efataa!" (Kutanthauza kuti,
"Tsekuka!") 35 Atachita izi, makutu a munthuyo anatsekuka komanso
lilime lake linamasuka ndipo anayamba kuyankhula momveka bwino.

36 Yesu anawalamula kuti asawuze wina aliyense. Koma pamene
anapitiriza kuwaletsa, iwo anapitiriza kuyankhula za izi. 37 Anthu
anadabwa kwambiri. Iwo anati, "Wachita zonse bwino, ngakhale Iyenso
atsekula makutu a osamva ndi osayankhula kuti ayankhule."

# 8

### *Yesu Adyetsa Anthu 4,000*

1 M'masiku amenewo gulu lina lalikulu la anthu linasonkhana. Popeza
iwo analibe chakudya, Yesu anayitana ophunzira ake nati kwa iwo, 2 "Ndili
ndi chifundo ndi anthu awa; akhala ali ndi Ine masiku atatuwa ndipo
alibe chakudya. 3 Ngati nditawawuza kuti apite kwawo ali ndi njala, iwo
adzakomoka m'njira chifukwa ena a iwo achokera kutali."

4 Ophunzira ake anayankha nati, "Kodi ndi kuti kuthengo kuno kumene
munthu angapeze buledi okwanira kuwadyetsa?"

5 Yesu anafunsa kuti, "Muli ndi malofu a buledi angati?"

Iwo anayankha kuti, "Asanu ndi awiri."

6 Iye anawuza gulu la anthu kuti likhale pansi. Atatenga malofu a buledi
asanu ndi awiri, anayamika, nawanyema ndipo anapatsa ophunzira ake
kuti agawire anthu, ndipo iwo anatero. 7 Analinso ndi tinsomba tochepa;
Iye anayamikanso chifukwa cha nsombazo. Ndipo anawuza ophunzira
kuti awagawire. 8 Anthu anadya ndipo anakhuta. Atamaliza, ophunzira
anatola buledi ndi nsomba zotsalira ndi kudzaza madengu asanu ndi
awiri. 9 Panali amuna pafupifupi 4,000. Ndipo atawawuza kuti apite
kwawo, 10 analowa m'bwato pamodzi ndi ophunzira ake napita ku dera
la Dalamanuta.

11 Afarisi anabwera nayamba kumufunsa Yesu. Pomuyesa Iye, anamu-
funsa za chizindikiro chochokera kumwamba. 12 Ndipo anatsitsa moyo
nati, "N'chifukwa chiyani m'bado uno ukufuna chizindikiro chodabwitsa?
Zoonadi, ndikuwuzani kuti palibe chizindikiro chidzapatsidwa kwa iwo."
13 Ndipo anawasiya, nalowanso m'bwato ndi kuwolokera tsidya lina.

### *Yisiti wa Afarisi ndi Herode*

14 Ophunzira anayiwala kutenga buledi, kupatula buledi mmodzi yekha
amene anali naye m'bwato. 15 Yesu anawachenjeza kuti, "Samalani ndipo
onetsetsani yisiti wa Afarisi ndi wa Herode."

16 Iwo anakambirana wina ndi mnzake ndipo anati, "Ndi chifukwa choti
tilibe buledi."

17 Yesu atadziwa zokambirana zawo anawafunsa kuti, "N'chifukwa
chiyani mukukambirana kuti mulibe buledi? Kodi inu simukuonabe
kapena kuzindikira? Kodi mitima yanu ndi yowumitsidwa? 18 Kodi muli
ndi maso ndipo simukuona, ndi makutu ndipo mukulephera kumva? Kodi
simukukumbukira? 19 Pamene ndinagawa malofu asanu a buledi kwa
anthu 5,000, ndi madengu angati amene munatoleramo buledi ndi nsomba
zotsalira?"

Iwo anayankha kuti, "Khumi ndi awiri."

20 "Ndipo pamene ndinagawa malofu asanu ndi awiri a buledi, kwa anthu 4,000, ndi madengu angati amene munatoleramo buledi ndi nsomba zotsalira?"

Iwo anayankha kuti, "Asanu ndi awiri."

21 Iye anawafunsa kuti, "Kodi simumvetsetsabe?"

### *Kuchiritsidwa kwa Munthu Wosaona ku Betisaida*

22 Iwo anafika ku Betisaida, ndipo anthu ena anabweretsa munthu
wosaona ndipo anamupempha Yesu kuti amukhudze. 23 Iye anagwira
dzanja la munthu wosaonayo napita naye kunja kwa mudzi. Atalavulira m'maso a munthuyo ndi kumusanjika manja, Yesu anafunsa kuti, "Kodi ukuona kalikonse?"

24 Iye anakweza maso nati, "Ndikuona anthu; akuoneka ngati mitengo imene ikuyendayenda."

25 Kenakanso Yesu anayika manja ake m'maso a munthuyo. Ndipo maso
ake anatsekuka, naonanso, ndipo anaona zonse bwinobwino. 26 Yesu
anamuwuza kuti apite kwawo nati, "Usapite m'mudzimo."

### *Petro Avomereza Khristu*

27 Yesu ndi ophunzira ake anapita ku midzi yozungulira Kaisareya wa Filipo. Ali panjira, Iye anawafunsa kuti, "Kodi anthu amati ndine yani?"

28 Iwo anayankha kuti, "Ena amati Yohane M'batizi; ena amati Eliya; ndipo enanso amati ndinu mmodzi wa aneneri."

29 Iye anafunsa kuti, "Koma nanga inu, mumati ndine yani?"

Petro anayankha kuti, "Inu ndinu Khristu."

30 Yesu anawachenjeza kuti asawuze wina aliyense za Iye.

### *Yesu Aneneratu za Imfa Yake*

31 Iye anayamba kuwaphunzitsa kuti, "Mwana wa Munthu ayenera
kumva zowawa zambiri ndi kukanidwa ndi akulu a ansembe, ndi
aphunzitsi a malamulo, ndi kuti ayenera kuphedwa ndipo patatha masiku
atatu adzaukanso." 32 Izi anaziyankhula momveka bwino, ndipo Petro
anamutengera pambali ndipo anayamba kumudzudzula.

33 Koma Yesu atatembenuka ndi kuyang'ana ophunzira ake, anamudzudzula Petro nati, "Choka pamaso panga Satana! Suganizira zinthu za Mulungu koma za anthu."

### *Njira ya Mtanda*

34 Kenaka anayitana gulu la anthu pamodzi ndi ophunzira ake nati:
"Ngati wina aliyense afuna kunditsata Ine, ayenera kudzikana yekha ndi
kunyamula mtanda wake ndi kunditsata. 35 Pakuti aliyense amene afuna
kupulumutsa moyo wake adzawutaya, koma aliyense amene ataya moyo
wake chifukwa cha Ine ndi cha Uthenga Wabwino, adzawupulumutsa.
36 Kodi munthu adzapindulanji akalandira dziko lonse lapansi, koma ndi
kutaya moyo wake? 37 Kapena n'chiyani chomwe munthu angapereke
chosinthana ndi moyo wake? 38 Ngati wina achita manyazi chifukwa cha
Ine ndi mawu anga mu m'bado uno wachigololo ndi wochimwa, Mwana wa Munthu adzachita naye manyazi pamene adzabwera mu ulemerero wa Atate ake pamodzi ndi angelo oyera."

# 9

1 Ndipo anawawuza kuti, "Zoonadi, ndikuwuzani kuti ena amene
ayimirira pano sadzafa asanaone ufumu wa Mulungu ukubwera mwa
mphamvu."

### *Maonekedwe a Ulemerero wa Yesu pa Phiri*

2 Patatha masiku asanu ndi limodzi Yesu anatenga Petro, Yakobo ndi
Yohane nawatsogolera kupita ku phiri lalitali, kumene anali okhaokha.
Kumeneko maonekedwe ake anasinthika pamaso pawo. 3 Zovala zake
zinawala monyezimira kwambiri, kotero kuti palibe sopo wina aliyense
amene angaziyeretse monyezimira chotere pa dziko la pansi. 4 Ndipo
anaonekera Eliya ndi Mose pamaso pawo, amene ankayankhulana ndi
Yesu.

5 Petro anati kwa Yesu, "Aphunzitsi, ndi kwabwino kuti ife tili pano.
Tiyeni timange misasa itatu; umodzi wanu, wina wa Mose ndi wina wa
Eliya." 6 (Iye sanadziwe choti anene, anali ndi mantha akulu).

7 Pamenepo mtambo unaoneka ndi kuwaphimba, ndipo mawu
anamveka kuchokera mu mtambo kuti, "Uyu ndi Mwana wanga wokondedwa. Mvereni Iye!"

8 Mwadzidzidzi, atayang'anayang'ana, sanaonenso wina aliyense ali ndi
iwo kupatula Yesu.

9 Pamene ankatsika kuchokera ku phiri, Yesu anawalamulira kuti
asawuze aliyense zimene anaona mpaka Mwana wa Munthu atauka kwa
akufa. 10 Iwo anayisunga nkhaniyo nakambirana za tanthauzo lake la
"Kuuka kwa akufa."

11 Ndipo anamufunsa Iye kuti, "N'chifukwa chiyani aphunzitsi amalamulo amati Eliya ayenera kuyamba wabwera?"

12 Yesu anayankha kuti, "Kunena motsimikiza, Eliya ayeneradi kuyamba
kubwera kudzakonzanso zinthu zonse. N'chifukwa chiyani tsono zinalembedwa, kuti Mwana wa Munthu ayenera kuvutika kwambiri ndi
kukanidwa? 13 Koma ndikuwuzani, kuti Eliya wabweradi, ndipo amuchitira iye zonse zimene iwo anafuna, monga momwe zalembedwera za iye."

### *Kuchiritsidwa kwa Mnyamata Wogwidwa ndi Mzimu Woyipa*

14 Atafika kwa ophunzira ena aja, anaona gulu lalikulu la anthu
litawazungulira ndi aphunzitsi amalamulo akutsutsana nawo. 15 Nthawi
yomweyo anthu onse atamuona, anadabwa kwambiri ndipo anathamanga
kukamulonjera.

16 Iye anafunsa kuti, "Mukukangana nawo chiyani iwowa?"

17 Munthu wina m'gululo anayankha kuti, "Aphunzitsi, ndinakubweretserani mwana wanga wamwamuna, amene ndi ogwidwa ndi mzimu
umene umamulepheretsa kuyankhula. 18 Nthawi iliyonse ukamugwira
umamugwetsa pansi. Amatuluka thovu kukamwa, amakukuta mano
ake ndipo amawuma. Ndinapempha ophunzira anu kuti awutulutse
mzimuwo, koma sanathe."

19 Yesu anayankha kuti, "Haa! M'bado osakhulupirira, kodi ndidzakhala
nanu mpaka liti? Mubweretseni kwa Ine mnyamatayo."

20 Ndipo anamubweretsa kwa Iye. Mzimu woyipawo utaona Yesu,
nthawi yomweyo unamukomola mnyamatayo. Anagwa pansi ndi kumagubuduka, ndi kuchita thovu kukamwa.

21 Yesu anafunsa abambo a mnyamatayo kuti, "Kodi wakhala chotere
nthawi yayitali bwanji?"

Iye anayankha kuti, “Kuyambira ali wamng’ono, 22 wakhala
ukumuponya pa moto kapena m’madzi kuti umuphe. Koma ngati
mungathe kuchita kanthu, tichitireni chifundo ndipo mutithandize.”
23 Yesu anati, “ ‘Ngati mungathe!’ Zinthu zonse ndi zotheka kwa iye
amene akhulupirira.”
24 Nthawi yomweyo abambo a mwanayo anafuwula kuti,
“Ndikhulupirira; thandizani kusakhulupirira kwanga!”
25 Yesu ataona kuti gulu la anthu likuthamangira kumalowo,
anadzudzula mzimu woyipawo kuti, “Iwe mzimu wolepheretsa
kuyankhula ndi kumva, ndikulamulira tuluka mwa iye ndipo
usadzalowenso.”
26 Mzimuwo unafuwula ndi kumugubuduza kwambiri ndipo unatuluka.
Mnyamatayo anaoneka ngati mtembo ndipo ambiri anati, “Wafa.” 27 Koma
Yesu anamugwira dzanja ndipo anamuyimiritsa, ndipo anayimirira.
28 Yesu atalowa m’nyumba, ophunzira ake anamufunsa ali pa okha kuti,
“Kodi ndi chifukwa chiyani ife sitinathe kutulutsa chiwandacho?”
29 Iye anayankha kuti, “Mtundu uwu umatuluka pokhapokha mwapem-
phera ndi kusala kudya.”

### *Yesu aneneratu za Imfa yake Kachiwiri*

30 Anachoka malo amenewo nadutsa ku Galileya. Yesu sanafune
kuti wina aliyense adziwe kumene anali, 31 chifukwa amaphunzitsa
ophunzira ake. Anati kwa iwo, “Mwana wa Munthu adzaperekedwa
m’manja mwa anthu. Adzamupha, ndipo patatha masiku atatu adzauka.”
32 Koma sanazindikire chimene amatanthauza, ndipo anachita mantha
kuti amufunse.

### *Wamkulu Ndani mu Ufumu wa Mulungu?*

33 Anafika ku Kaperenawo. Pamene anali m’nyumba, anawafunsa kuti,
“Kodi mumatsutsana chiyani m’njira muja?” 34 Koma anakhala chete
chifukwa ali m’njira amatsutsana za kuti wamkulu kuposa onse ndani.
35 Atakhala pansi, Yesu anayitana khumi ndi awiriwo nati, “Ngati
wina aliyense afuna kukhala woyamba, ayenera kukhala wotsiriza ndi
wotumikira onse.”
36 Anatenga kamwana nakayimiritsa pakati pawo ndipo anawawuza
kuti, 37 “Aliyense wolandira mmodzi wa ana ang’ono awa m’dzina langa
alandira Ine; ndipo aliyense wolandira Ine salandira Ine koma amene
ananditumа.”

### *Wosatsutsana Nafe Athandizana Nafe*

38 Yohane anati, “Aphunzitsi, tinaona munthu akutulutsa ziwanda
m’dzina lanu ndipo ife tinamuwuza kuti aleke, chifukwa sanali mmodzi
wa ife.”
39 Yesu anati, “Musamuletse, palibe amene amachita chodabwitsa
m’dzina langa ndipo kenaka nanena zoyipa za Ine, 40 pakuti aliyense
amene satsutsana nafe ali mbali yathu. 41 Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti
aliyense amene akupatsani chikho cha madzi m’dzina langa chifukwa
ndinu ake a Khristu, sadzataya konse mphotho yake.”

### *Zochimwitsa Ena*

42 “Ndipo ngati wina aliyense achimwitsa mmodzi wa ana ang’ono awa
amene akhulupirira Ine, kukanakhala bwino kwa iye kuti aponyedwe
m’nyanja atamangiriridwa mwala waukulu m’khosi mwake. 43 Ngati

dzanja lako likuchimwitsa, lidule. Ndi kwabwino kwa iwe kulowa m'moyo
ndi dzanja limodzi kusiyana ndi kukhala ndi manja awiri ndi kupita ku
gehena, kumene moto wake suzima. 44 (Kumene mphutsi zake sizifa ndipo
moto wake suzima). 45 Ndipo ngati phazi lako likuchimwitsa, lidule. Ndi
kwabwino kwa iwe kulowa m'moyo olumala kusiyana ndi kukhala ndi
mapazi awiri ndi kuponyedwa mu gehena. 46 (Kumene mphutsi zake
sizifa ndipo moto wake suzima). 47 Ndipo ngati diso lako likuchimwitsa,
likolowole. Ndi kwabwino kwa iwe kulowa ufumu wa Mulungu ndi
diso limodzi, kusiyana ndi kukhala ndi maso awiri ndi kuponyedwa mu
gehena, 48 kumene

" 'mphutsi zake sizifa
ndipo moto wake suzima.'

49 Aliyense adzayesedwa ndi moto.

50 "Mchere ndi wabwino, koma ngati utasukuluka, mungawukol-
eretsenso bwanji? Mukhale nawo mchere mwa inu nokha, ndipo mukhale
pa mtendere wina ndi mnzake."

# 10

*Za Kusudzula*

1 Ndipo Yesu anachoka pamalowo ndi kupita kudera la Yudeya ndi
kutsidya la mtsinje wa Yorodani. Magulu a anthu anabweranso kwa Iye,
ndipo monga mwachizolowezi chake anawaphunzitsa.

2 Afarisi ena anabwera kudzamuyesa pomufunsa kuti, "Kodi malamulo
amalola kuti mwamuna asiye mkazi wake?"

3 Iye anayankha kuti, "Kodi Mose anakulamulani chiyani?"

4 Iwo anati, "Mose amaloleza mwamuna kulemba kalata ya chisudzulo
ndi kumuchotsa mkazi."

5 Yesu anayankha kuti, "Mose anakulemberani lamulo ili chifukwa
chakuwuma kwa mitima yanu. 6 Koma pachiyambi cha chilengedwe,
Mulungu 'analenga iwo, mwamuna ndi mkazi.' 7 'Pa chifukwa ichi
mwamuna adzasiya abambo ake ndi amayi ake nakaphatikana ndi mkazi
wake, 8 ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi.' Potero sali awirinso,
koma mmodzi. 9 Chifukwa chake chimene Mulungu wachilumikiza
pamodzi, munthu wina asachilekanitse."

10 Pamene analinso m'nyumba, ophunzira anamufunsa Yesu za izi. 11 Iye
anayankha kuti, "Aliyense amene aleka mkazi wake ndi kukakwatira wina
achita chigololo kulakwira mkaziyo. 12 Ndipo akasiya mwamuna wake ndi
kukakwatiwa ndi wina, achita chigololo."

*Yesu Adalitsa Ana*

13 Anthu anabweretsa ana kwa Yesu kuti awadalitse, koma ophunzira
anawadzudzula. 14 Pamene Yesu anaona zimenezi anayipidwa. Anati kwa
iwo, "Lolani ana abwere kwa Ine, ndipo musawaletse, pakuti Ufumu wa
Mulungu uli wa onga awa. 15 Ndikukuwuzani choonadi, aliyense amene
sadzalandira Ufumu wa Mulungu ngati kamwana sadzalowamo." 16 Ndipo
ananyamula ana m'manja ake, ndi kuyika manja ake pa iwo nawadalitsa.

*Munthu Wachuma ndi Ufumu wa Mulungu*

17 Yesu atanyamuka, munthu wina anamuthamangira nagwa mogwada
pamaso pake. Iye anafunsa kuti, "Aphunzitsi abwino, ndichite chiyani kuti
ndilandire moyo wosatha?"

18 Yesu anamufunsa kuti, “N’chifukwa chiyani ukunditchula wabwino?
Palibe wabwino koma Mulungu yekha. 19 Iwe umadziwa malamulo:
‘Usaphe, usachite chigololo, usabe, usapereke umboni wonama, usachite
chinyengo, lemekeza abambo ndi amayi ako.’ ”
20 Iye anati, “Aphunzitsi zonsezi ndinazisunga kuyambira ndili mnyamata.”
21 Yesu anamuyang’ana ndi kumukonda nati, “Ukusowa chinthu chimodzi. Pita, kagulitse zonse zimene uli nazo ndipo kapereke kwa osauka,
ndipo udzakhala ndi chuma kumwamba. Ndipo ukabwere ndi kunditsata
Ine.”
22 Pa chifukwa ichi nkhope yake inagwa. Anachoka ali wachisoni,
chifukwa anali ndi chuma chambiri.
23 Yesu anayang’anayang’ana ndipo anati kwa ophunzira ake,
“N’kovutadi kuti achuma akalowe mu ufumu wa Mulungu!”
24 Ophunzira anadabwa ndi mawu ake. Koma Yesu anatinso, “Ananu,
n’kovutadi kulowa mu ufumu wakumwamba! 25 Ndi kwapafupi kwa
ngamira kuti idzere pa kabowo ka zingano kusiyana ndi munthu wachuma
kuti alowe mu ufumu wa Mulungu.”
26 Ophunzira anadabwa kwambiri, ndipo anati kwa wina ndi mnzake,
“Nanga ndani amene angapulumuke?”
27 Yesu anawayang’ana ndipo anati, “Kwa munthu zimenezi
n’zosatheka, koma osati ndi Mulungu; zinthu zonse zimatheka ndi
Mulungu.”
28 Petro anati kwa Iye, “Ife tasiya zonse ndi kukutsatani!”
29 Yesu anayankha kuti, “Zoonadi, ndikuwuzani kuti palibe aliyense
amene wasiya nyumba kapena abale kapena alongo kapena amayi
kapena abambo kapena ana kapena minda chifukwa cha Ine ndi Uthenga
Wabwino 30 adzalephera kulandira 100 (nyumba, abale, alongo, amayi,
ana ndi minda, pamodzi ndi mazunzo) m’bado uno ndi moyo wosatha
nthawi ya m’tsogolo. 31 Koma ambiri amene ndi woyambirira adzakhala
omalizira, ndipo omalizira adzakhala oyambirira.”

### *Yesu Aneneratunso za Imfa Yake*

32 Ali pa ulendo wawo wopita ku Yerusalemu, Yesu ali patsogolo,
ophunzira ake anadabwa, ndipo amene amamutsatira amachita mantha.
Anatenganso ophunzira ake khumi ndi awiri pa mbali ndipo anawawuza
zimene zikamuchitikire Iye. 33 Iye anati, “Ife tikupita ku Yerusalemu ndipo
Mwana wa Munthu adzaperekedwa kwa akulu a ansembe ndi aphunzitsi
amalamulo. Adzamuweruza kuti aphedwe ndipo adzamupereka kwa
anthu a mitundu ina, 34 amene adzamuchita chipongwe ndi kumuthira
malovu, kumukwapula ndi kumupha. Patatha masiku atatu adzauka.”

### *Pempho la Yakobo ndi Yohane*

35 Ndipo Yakobo ndi Yohane, ana a Zebedayo, anabwera kwa Iye ndipo
anati, “Aphunzitsi, tikufuna kuti mutichitire ife chilichonse chimene
tipemphe.”
36 Iye anafunsa kuti, “Kodi mukufuna ndikuchitireni chiyani?”
37 Iwo anayankha kuti, “Timafuna kuti mmodzi wa ife adzakhale
kumanja ndi wina kumanzere mu ulemerero wanu.”
38 Yesu anati, “Simukudziwa chimene mukupempha. Kodi mungamwere
chikho chimene ndidzamwera kapena kubatizidwa ndi ubatizo umene
ndibatizidwe nawo?”

39 Iwo anayankha kuti, “Tikhoza.” Yesu anawawuza kuti, “Mudzamw-
eradi chikho chimene Ine ndidzamwera, ndi kubatizidwa ndi ubatizo
umene Ine ndidzabatizidwe nawo, 40 koma kukhala kumanja kapena
kumanzere si Ine wopereka. Malo awa ndi a amene anasankhidwiratu.”
41 Ophunzira khumiwo otsalawo atamva izi anapsera mtima Yakobo
ndi Yohane. 42 Yesu anawayitana pamodzi nati, “Inu mukudziwa kuti
iwo amene amadziyesa ngati atsogoleri a anthu amitundu ina amadyera
anthu awo masuku pamutu. Akuluakulu awonso amaonetsadi mphamvu
zawo pa iwo. 43 Sizili choncho ndi inu. M’malo mwake, amene akufuna
kukhala wamkulu pakati panu ayenera kukhala wotumikira, 44 ndipo
aliyense amene akufuna kukhala wamkulu akhale kapolo wa onse.
45 Pakuti ngakhale Mwana wa Munthu sanabwere kudzatumikiridwa,
koma kudzatumikira, ndi kupereka moyo wake kuti ukhale dipo la anthu
ambiri.”

### *Bartumeyu Wosaona*

46 Ndipo anafika ku Yeriko. Pamene Yesu ndi ophunzira ake, pamodzi
ndi gulu lalikulu la anthu, ankatuluka mu mzinda, munthu wosaona,
Bartumeyu (mwana wa Tumeyu), amakhala m’mbali mwa msewu ali
kupempha. 47 Pamene anamva kuti anali Yesu wa ku Nazareti, anayamba
kufuwula kuti, “Yesu, Mwana wa Davide, mundichitire chifundo!”
48 Ambiri anamukalipira ndi kumuwuza kuti akhale chete, koma iye
anafuwulitsabe kuti, “Mwana wa Davide, mundichitire chifundo!”
49 Yesu anayima nati, “Muyitaneni.” Ndipo anamuyitana kuti, “Kondw-
era! Imirira! Akukuyitana.” 50 Anaponya mkanjo wake kumbali,
analumpha nabwera kwa Yesu.
51 Yesu anamufunsa kuti, “Ukufuna ndikuchitire chiyani?”

Wosaonayo anayankha kuti, “Aphunzitsi, ndikufuna ndione.”

52 Yesu anati, “Pita, chikhulupiriro chako chakuchiritsa!” Nthawi
yomweyo anapenya, n’kumatsatira Yesu pa ulendowo.

## 11

### *Yesu Alowa mu Yerusalemu Mwaulemerero*

1 Atayandikira ku Yerusalemu, anafika ku Betifage ndi Betaniya ku phiri
la Olivi. Yesu anatuma awiri a ophunzira ake 2 nati kwa iwo, “Pitani
ku mudzi uli patsogolo panu, ndipo mukamakalowa, mukapeza mwana
wabulu atamangiririridwa pamenepo, amene wina aliyense sanakwerepo.
Kamumasuleni ndi kubwera naye kuno. 3 Ngati wina aliyense akaku-
funsani kuti, ‘Mukuchita zimenezi chifukwa chiyani?’ Kamuwuzeni kuti,
‘Ambuye akumufuna ndipo akamutumiza kuno msanga.’ ”
4 Anapita ndipo anakapeza mwana wabulu ali kunja mu msewu
waukulu atamumangirira pa chipata. Pamene anamumasula, 5 anthu ena
amene anayima pomwepo anafunsa kuti, “Mukuchita chiyani, kumasula
mwana wabuluyo?” 6 Iwo anayankha monga mmene Yesu anawawuzira,
ndipo anthu aja anawalola kuti apite. 7 Atafika naye mwana wabulu
kwa Yesu, nayika mikanjo yawo pa buluyo, Iye anakwerapo. 8 Anthu
ambiri anayala mikanjo yawo pa msewu, pamene ena anayala nthambi
zomwe anadula m’minda. 9 Amene anatsogola ndi iwo amene ankatsatira
ankafuwula kuti,
“Hosana!

“Odala Iye amene akudza m’dzina la Ambuye!”

10 “Odala ndi ufumu umene ukubwera wa abambo athu Davide!”

“Hosana Mmwambamwamba!”
11 Yesu analowa mu Yerusalemu napita ku Nyumba ya Mulungu.
Anayang’ana zonse, koma popeza kuti nthawi inali itapita, anatuluka
kupita ku Betaniya pamodzi ndi khumi ndi awiriwo.

### *Yesu Atemberera Mkuyu*

12 Mmawa mwake pamene amachoka ku Betaniya, Yesu anamva njala.
13 Ataonera patali mtengo wamkuyu uli ndi masamba, anapita kuti akaone
ngati unali ndi chipatso chilichonse. Atafika, sanapezemo kanthu koma
masamba, chifukwa sinali nthawi ya nkhuyu. 14 Ndipo Iye anati kwa
mtengo, “Palibe amene adzadyenso chipatso kuchokera kwa iwe.” Ndipo
ophunzira ake anamva Iye akunena izi.

### *Yesu Ayeretsa Nyumba ya Mulungu*

15 Atafika ku Yerusalemu, Yesu analowa m’bwalo lakunja la Nyumba ya
Mulungu ndipo anayamba kupirikitsa anthu amene amagula ndi kugulitsa
m’menemo. Anagubuduza matebulo a osintha ndalama ndi mipando
ya ogulitsa nkhunda, 16 ndipo Iye sanalole aliyense kugulitsa malonda
m’mabwalo a Nyumba ya Mulungu. 17 Ndipo pamene ankawaphunzitsa,
Iye anati, “Kodi sikunalembedwe kuti, ‘Nyumba yanga idzatchedwa
Nyumba ya mapemphero kwa anthu a mitundu yonse?’ Koma inu
mwayisandutsa ‘phanga la achifwamba.’ ”
18 Akulu a ansembe ndi aphunzitsi amalamulo anamva izi ndipo
anayamba kufuna njira yoti amuphere Iye, pakuti amamuopa, chifukwa
gulu lonse la anthu linazizwa ndi chiphunzitso chake.
19 Pofika madzulo, iwo anatuluka mu mzindamo.

### *Mkuyu Wofota*

20 Mmamawa, pamene ankayenda, anaona mtengo wamkuyu uja utafota
kuyambira ku mizu. 21 Petro anakumbukira nati kwa Yesu, “Aphunzitsi,
taonani! Mtengo wamkuyu munawutemberera uja wafota!”
22 Yesu anayankha kuti, “Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.
23 Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti ngati wina aliyense angalamule phiri
ili kuti, ‘Pita, kadziponye m’nyanja,’ ndipo wosakayika mu mtima mwake
koma kukhulupirira kuti chimene akunena chidzachitika, chidzachitikadi
kwa iyeyo. 24 N’chifukwa chake ndikukuwuzani kuti chilichonse chimene
mupempha m’pemphero, khulupiririrani kuti mwalandira, ndipo chidza-
khala chanu. 25 Pamene muyimirira kupemphera, ngati muli ndi chifukwa
ndi wina, mukhululukireni, kuti Atate anu akumwamba akukhululukireni
machimo anu.” 26 (Koma ngati simukhululukirana, ngakhale Atate anu
akumwamba sadzakhululukira machimo anu).

### *Amufunsa Yesu za Ulamuliro Wake*

27 Iwo anafikanso ku Yerusalemu, ndipo pamene Yesu amayenda
m’mabwalo a Nyumba ya Mulungu, akulu a ansembe, aphunzitsi amala-
mulo ndi akuluakulu anabwera kwa Iye. 28 Iwo anafunsa kuti, “Mukuchita
izi ndi ulamuliro wanji? Ndipo anakupatsani ulamuliro umenewu ndi
ndani?”

29 Yesu anayankha kuti, “Ndikufunsani funso limodzi. Mundiyankhe,
ndipo ndikuwuzani ndi ulamuliro wanji umene ndikuchitira izi. 30 Ubatizo
wa Yohane, unali wochokera kumwamba, kapena kwa anthu? Ndi-
wuzeni.”
31 Iwo anakambirana pakati pawo ndipo anati, “Tikati, ‘Wochok-
era kumwamba,’ atifunsa kuti, ‘Nanga n’chifukwa chiyani simuna-
mukhulupirire?’ 32 Koma ife tikati, ‘Wochokera kwa anthu.’ ” (Amaopa
anthu, pakuti aliyense amakhulupirira kuti Yohane analidi mneneri).
33 Ndipo anamuyankha Yesu kuti, “Sitikudziwa.”
Yesu anati, “Nanenso sindikuwuzani kuti ndi ulamuliro wanji ndichitira
zimenezi.”

# 12

### *Fanizo la Alimi*

1 Kenaka Iye anayamba kuyankhula nawo m’mafanizo: “Munthu wina
analima munda wamphesa. Anamanga mpanda mozungulira, nakumba
dzenje lofinyiramo mphesa ndipo anamanga nsanja. Anawubwereketsa
munda wamphesawo kwa alimi ena napita ku dziko lina. 2 Pa nthawi
yokolola anatumiza wantchito kwa alimiwo kuti akatenge kuchokera kwa
iwo zina mwa zipatso za munda wamphesa. 3 Koma iwo anamugwira,
namumenya ndi kumupirikitsa wopanda kanthu. 4 Kenaka anatumizanso
wantchito wina kwa iwo. Iwo anamumenya munthuyo pamutu ndipo
anamuzunza mochititsa manyazi. 5 Anatumizanso wina, ndipo iwo
anamupha. Anatumizanso ena ambiri; ena a iwo anawamenya, ena
anawapha.
6 “Munthu uja anatsala ndi mwana mmodzi, wamwamuna amene
amamukonda. Pomaliza anamutumiza mwanayo nati, ‘Adzamuchitira
ulemu mwana wanga.’
7 “Koma alimi aja anati kwa wina ndi mnzake, ‘Uyu ndi mlowam’malo.
Tiyeni timuphe, ndipo cholowacho chidzakhala chathu.’ 8 Ndipo ana-
mutenga ndi kumupha, ndipo anamuponya kunja kwa munda wamphesa.
9 “Kodi nanga mwini munda wamphesa adzachita chiyani? Iye
adzabwera ndi kupha alimiwo nadzapereka munda wamphesawo kwa
ena. 10 Kodi simunawerenge lemba lakuti:
“ ‘Mwala umene amisiri omanga nyumba anawukana
wakhala mwala wa pa ngodya.
11 Ambuye achita zimenezi,
ndipo ndi zodabwitsa m’maso mwathu?’ ”
12 Ndipo akulu a ansembe, aphunzitsi a malamulo ndi akuluakulu ana-
funafuna njira yoti amugwirire Iye chifukwa amadziwa kuti anayankhula
fanizoli mowatsutsa iwo. Koma amaopa gulu la anthu; ndipo anamusiya
napita.

### *Za Kupereka Msonkho kwa Kaisara*

13 Pambuyo pake anatuma ena a Afarisi ndi Aherode kwa Yesu kuti
adzamukole mawu ake. 14 Iwo anabwera kwa Iye nati, “Aphunzitsi, ife
tikudziwa kuti Inu ndi munthu amene mumanena zoona. Inu simutengeka
ndi anthu, chifukwa simusamala kuti ndi ndani; koma mumaphunzitsa
njira ya Mulungu molingana ndi choonadi. Kodi ndi koyenera kupereka
msonkho kwa Kaisara kapena ayi? 15 Kodi ife tipereke msonkho kapena
ayi?”

Koma Yesu anadziwa chinyengo chawo. Iye anafunsa kuti, “Bwanji
mukufuna kundipeza chifukwa? Bweretsani ndalama kuti ndiyione.”
16 Iwo anamubweretsera ndalama, ndipo anawafunsa kuti, “Kodi nkhope
iyi ndi ya ndani? Nanga malembawa ndi a ndani?”

Iwo anayankha kuti, “Za Kaisara.”

17 Ndipo Yesu anawawuza kuti, “Perekani kwa Kaisara zake za Kaisara
ndi kwa Mulungu zake za Mulungu.”

Ndipo anazizwa naye.

### *Za Ukwati ndi Kuuka kwa Akufa*

18 Kenaka Asaduki, amene amati kulibe kuuka kwa akufa, anabwera kwa
Iye ndi funso. 19 Iwo anati, “Aphunzitsi, Mose anatilembera kuti munthu
akamwalira ndi kusiya mkazi wopanda ana, m’bale wa munthu wom-
walirayo akuyenera kukwatira mkaziyo kuti amuberekere ana m’bale
wakeyo. 20 Tsopano panali abale asanu ndi awiri. Woyamba anakwatira
namwalira wosabereka ana. 21 Wachiwiri anakwatira mkazi wamasiyeyo,
koma iye anamwalira wosabereka mwana. Zinali chimodzimodzi ndi
wachitatu. 22 Kunena zoona, palibe ndi mmodzi yemwe wa asanu ndi
awiriwo anasiya ana. Pomaliza, mkaziyo anamwaliranso. 23 Pa kuuka
kwa akufa, adzakhala mkazi wa yani pakuti anakwatiwa ndi onse asanu
ndi awiri?”

24 Yesu anawafunsa kuti, “Kodi si pamenepa nanga pomwe mumalak-
wira chifukwa simukudziwa malemba kapena mphamvu za Mulungu?
25 Pamene akufa auka, sadzakwatira kapena kukwatiwa; adzakhala ngati
angelo kumwamba. 26 Tsopano kunena zakuti akufa amauka, kodi
simunawerenge m’buku la Mose, pa nkhani yachitsamba choyaka moto,
mmene Mulungu anati kwa iye, ‘Ine ndine Mulungu wa Abrahamu,
Mulungu wa Isake, ndi Mulungu wa Yakobo?’ 27 Iye si Mulungu wa anthu
akufa, koma wa amoyo. Inu mwalakwitsa kwambiri!”

### *Lamulo Lalikulu Koposa*

28 Mmodzi wa aphunzitsi amalamulo anabwera namva iwo akukam-
birana motsutsana. Poona kuti Yesu anawapatsa yankho labwino,
anamufunsa Iye kuti, “Mwa malamulo onse, kodi lopambana koposa ndi
liti?”

29 Yesu anayankha kuti, “Lamulo loposa onse ndi ili: ‘Tamvani inu
Aisraeli! Yehova Mulungu wathu, Yehova ndi mmodzi! 30 Uzikonda Yehova
Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru
zako zonse ndi mphamvu zako zonse.’ 31 Lachiwiri ndi ili: ‘Konda mnansi
wako monga iwe mwini.’ Palibe lamulo lina loposa amenewa.”

32 Munthuyo anayankha kuti, “Mwanena bwino Aphunzitsi. Mwalon-
dola ponena kuti Mulungu ndi mmodzi ndipo palibe wina wofanana naye
koma Iye yekha. 33 Kumukonda Iye; ndi mtima wako wonse, ndi nzeru
zako zonse, ndi mphamvu zako zonse, ndi kukonda mnansi wako monga
iwe mwini, ndi zopambana kuposa zopereka ndi nsembe zopsereza.”

34 Yesu ataona kuti wayankha mwanzeru, anati kwa iye, “Iwe suli kutali
ndi ufumu wa Mulungu.” Ndipo kuyambira pamenepo panalibe ndi
mmodzi yemwe anayesa kumufunsanso.

### *Khristu ndi Mwana wa Yani?*

35 Yesu akuphunzitsa m’mabwalo a Nyumba ya Mulungu, anafunsa kuti,
“N’chifukwa chiyani aphunzitsi amalamulo amanena kuti, ‘Khristu ndi

Mwana wa Davide?’ 36 Pajatu Davide mwini wake, poyankhula mwa
Mzimu Woyera, ananena kuti,
“Ambuye anati kwa Ambuye anga:
‘Khalani pa dzanja langa lamanja
kufikira nditayika adani anu
pansi pa mapazi anu.’
37 Davide mwini wake amutchula Iye, ‘Ambuye.’ Nanga angakhale bwanji
mwana wake?”
Gulu lalikulu la anthu linamvetsera ndi chisangalalo.

### *Yesu Achenjeza Anthu za Aphunzitsi a Malamulo*

38 Pamene ankaphunzitsa, Yesu anati, “Samalani ndi aphunzitsi a mala-
mulo. Amakonda kuyendayenda atavala mikanjo ikuluikulu ndi kumalon-
jeredwa m’misika. 39 Ndipo amakhala pa mipando yofunika kwambiri
m’masunagoge ndi malo aulemu pa maphwando. 40 Amawononga
chuma cha akazi amasiye ndiponso amapemphera mapemphero aatali
odzionetsera. Anthu oterewa adzalangidwa kwambiri.”

### *Chopereka cha Mayi Wamasiye*

41 Yesu anakhala pansi moyang’anana ndi pamene amaperekera zop-
ereka ndipo amaona anthu akupereka ndalama zawo m’thumba la
Nyumba ya Mulungu. Anthu ambiri olemera anaponya ndalama zambiri.
42 Koma mkazi wamasiye, wosauka anabwera ndi kuyikamo tindalama
tiwiri ta kopala, tongokwanira theka la ndalama.
43 Yesu anayitana ophunzira ake nati, “Zoonadi, ndikuwuzani kuti mayi
wosauka wamasiyeyu waponya zambiri m’thumbali kuposa ena onsewa.
44 Iwo apereka molingana ndi chuma chawo; koma iye, mwaumphawi
wake, wapereka zonse anali nazo ngakhale zoti akanagulira chakudya.”

# 13

### *Zizindikiro za Kutha kwa Masiku Yomaliza*

1 Iye atachoka m’Nyumba ya Mulungu, mmodzi wa ophunzira ake
anati kwa Iye, “Aphunzitsi taonani! Miyala ikuluikulu! Nyumba
zikongolerenji!”
2 Yesu anayankha kuti, “Kodi mukuziona nyumba zikuluzikuluzi?
Palibe mwala ndi umodzi pano umene udzakhala pa unzake; uliwonse
udzagwetsedwa pansi.”
3 Yesu atakhala pansi pa phiri la Olivi moyang’anana ndi Nyumba ya
Mulungu, Petro, Yakobo, Yohane ndi Andreya anamufunsa Iye pambali
kuti, 4 “Tatiwuzani, izi zidzachitika liti? Nanga chizindikiro chakuti zatsala
pang’ono kukwaniritsidwa chidzakhala chiyani?”
5 Yesu anawawuza kuti, “Chenjerani kuti wina asakunyengeni. 6 Anthu
ambiri adzabwera m’dzina langa, nadzati, ‘Ine ndi Iyeyo,’ ndipo
adzanamiza anthu ambiri. 7 Pamene mudzamva zankhondo ndi mbiri
zankhondo, musadzadzidzimuke. Zinthu zotere ziyenera kuchitika, koma
sikuti chimaliziro chafika kale ayi. 8 Mtundu udzawukira mtundu unzake,
ndi ufumu kuwukira ufumu unzake. Kudzakhala zivomerezi m’malo
osiyanasiyana, ndi njala. Izi ndi chiyambi chabe cha zowawa monga mayi
pobereka.
9 “Muyenera kukhala tcheru. Mudzaperekedwa ku mabwalo oweruza
ndi kukwapulidwa mwankhanza m’masunagoge. Mudzayima pamaso
pa abwanamkubwa ndi mafumu monga mboni kwa iwo chifukwa cha

Ine. [10] Ndipo Uthenga Wabwino uyenera kuyamba walalikidwa kwa
anthu a mitundu yonse. [11] Nthawi iliyonse pamene mwamangidwa ndi
kuyimbidwa mlandu, musadandaule za zimene mudzanena. Zimene
mudzapatsidwe pa nthawiyo yankhulani; pakuti sindinu amene mudza-
yankhula, koma Mzimu Woyera.
[12] "M'bale adzapereka m'bale kuti aphedwe, ndipo abambo adzapereka
mwana wawo. Ana adzawukira makolo awo ndi kuwapereka kuti
aphedwe. [13] Anthu onse adzakudani chifukwa cha Ine, koma amene
adzalimbika mpaka potsiriza, ameneyo ndiye adzapulumuke.
[14] "Mukadzaona 'chinthu chonyansa chosakaza' chitayima pa malo
amene si ake, owerenga azindikire. Pamenepo amene ali ku Yudeya
athawire kumapiri. [15] Aliyense amene ali pa denga la nyumba
yake asatsike kapena kulowa m'nyumba kukatenga kanthu kalikonse.
[16] Aliyense amene ali ku munda asabwerere kukatenga mkanjo wake.
[17] Kudzakhala koopsa m'masiku amenewo kwa amayi oyembekezera ndi
amayi oyamwitsa! [18] Pempherani kuti zimenezi zisadzachitike nthawi
yozizira, [19] chifukwa masiku amenewo adzakhala owawitsa osafanana ndi
ena kuyambira pachiyambi, pamene Mulungu analenga dziko, kufikira
lero ndipo sadzafanananso ndi ena. [20] Ambuye akanapanda kufupik-
itsa masikuwo, palibe amene akanapulumuka. Koma chifukwa cha
osankhidwiratu, amene anawasankha, Iye anawafupikitsa. [21] Pa nthawi
imeneyo, ngati wina adzati kwa inu, 'Taonani, Khristu ali kuno, kapena,
Taonani, uyo ali apoyo!' musakhulupirire. [22] Pakuti akhristu onama ndi
aneneri onama adzaonekera ndipo adzachita zizindikiro ndi zodabwitsa
kuti anyenge osankhidwiratu ngati kutakhala kotheka kutero. [23] Choncho
khalani tcheru; ndakuwuzani zonse nthawi isanafike.
[24] "Koma masiku amenewo, masautsowo atatha,
" 'dzuwa lidzada,
ndipo mwezi sudzawala;
[25] nyenyezi zidzagwa kuchokera ku thambo,
ndipo mayiko mumlengalenga adzagwedezeka!'
[26] "Nthawi imeneyo anthu adzaona Mwana wa Munthu akubwera
m'mitambo ndi mphamvu yayikulu ndi ulemerero. [27] Ndipo adzatuma
angelo ake kukasonkhanitsa osankhidwiratu ake ku mphepo zinayi,
kuyambira kumalekezero a dziko lapansi mpaka ku malekezero ake
enanso.
[28] "Tsopano phunzirani phunziro ili kuchokera ku mtengo wamkuyu.
Pamene msonga za nthambi zake zikhala za nthete ndipo masamba ake
ayamba kuphukira, mumadziwa kuti dzinja layandikira. [29] Momwenso
pamene muona zinthu izi zikuchitika, dziwani kuti wayandikira, ali pa
khomo. [30] Zoonadi, Ine ndikuwuzani kuti m'bado uno sudzatha mpaka
zinthu zonsezi zitachitika. [31] Kumwamba ndi dziko lapansi zidzatha, koma
mawu anga sadzatha."

### *Tsiku ndi Ora Sizikudziwika*

[32] "Palibe amene akudziwa za tsikulo kapena nthawi, ngakhale angelo
akumwamba, kapena Mwana, koma Atate wokha. [33] Khalani maso!
Khalani tcheru! Simudziwa pamene nthawi imeneyo idzafike. [34] Zili
ngati munthu amene akuchokapo. Amasiyira nyumba yake antchito ake,
aliyense ndi ntchito yake; ndi kumuwuza wa pa khomo kuti azikhala maso.
[35] "Inunso muyenera kukhala maso chifukwa simukudziwa nthawi
imene mwini nyumba adzabwere, kaya madzulo, kapena pakati pa

usiku, kapena tambala akulira, kapena m'bandakucha. 36 Ngati atabwera
mwadzidzidzi, asadzakupezeni inu muli mtulo. 37 Zimene ndikunena kwa
inu, ndikunena kwa aliyense: 'Khalani tcheru!' "

# 14

### *Yesu Adzozedwa ku Betaniya*

1 Tsopano panali patatsala masiku awiri okha kuti tsiku la Paska ndi
Phwando la Buledi wopanda yisiti lifike, ndipo akulu a ansembe ndi
aphunzitsi amalamulo ankafunafuna mpata woti amugwire Yesu ndi
kumupha. 2 Iwo anati, "Koma osati nthawi yaphwando, chifukwa anthu
angachite chiwawa."

3 Pamene Iye anali m'Betaniya, atakhala pa tebulo akudya m'nyumba
ya munthu wodziwika kuti Simoni wakhate, anabwera mayi ndi botolo la
mafuta onunkhira amtengo wapamwamba opangidwa ndi nadi. Anaph-
wanya botololo nakhuthula mafutawo pa mutu wa Yesu.

4 Ena mwa iwo amene analipo, anakwiya nati kwa wina ndi mnzake,
"Chifukwa chiyani akuwononga mafuta onunkhirawa? 5 Akanatheka
kugulitsidwa ndi ndalama zambiri zoposa malipiro a pa chaka ndipo
ndalamazo ndi kupatsa osauka." Ndipo anamudzudzula iye mwaukali.

6 Yesu anati, "Musiyeni, chifukwa chiyani mukumuvutitsa? Wandichi-
tira Ine chinthu chabwino. 7 Anthu osauka mudzakhala nawo nthawi
zonse, ndipo mukhoza kuwathandiza nthawi iliyonse mungafune. Koma
simudzakhala ndi Ine nthawi zonse. 8 Wachita zimene akanatha. Wathira
mafuta onunkhira pa thupi langa nthawi isanakwane kukonzekera
kuyikidwa kwanga m'manda. 9 Zoonadi, ndikuwuzani kuti kulikonse
kumene Uthenga Wabwino udzalalikidwa pa dziko lonse, zimene wachi-
tazi zidzanenedwa pomukumbukira iye."

10 Kenaka Yudasi Isikarioti, mmodzi mwa khumi ndi awiriwo, anapita
kwa akulu a ansembe kuti akamupereke Yesu. 11 Iwo anakondwa
pakumva zimenezi ndipo analonjeza kumupatsa iye ndalama. Ndipo
ankadikira mpata wabwino woti amupereke.

### *Mgonero wa Ambuye*

12 Pa tsiku loyamba la Phwando la Buledi wopanda yisiti, nthawi imene
mwa mwambo inali ya kupha mwana wankhosa wa Paska, ophunzira a
Yesu anafunsa Iye kuti, "Mufuna tipite kuti kumene tikakonzekere kuti
mukadyere Paska?"

13 Pamenepo anatumiza awiri mwa ophunzira ake, nawawuza kuti,
"Pitani mu mzinda, ndipo mukakumana ndi mwamuna wonyamula
mtsuko wa madzi. Kamutsatireni iye. 14 Kawuzeni mwini nyumba
imene iye akalowemo kuti, 'Aphunzitsi akufunsa: kodi chili kuti chipinda
changa cha alendo, kumene ndidyere Paska ndi ophunzira anga?' 15 Iye
adzakuonetsani chipinda chachikulu chapamwamba, chokhala kale ndi
zonse ndi chokonzedwa kale. Katikonzereni ife Paska kumeneko."

16 Ophunzirawo anachoka, napita mu mzindawo ndipo anakapeza
zinthu monga mmene Yesu anawawuzira. Choncho anakakonza Paska.

17 Ndipo kutada Yesu anafika ndi khumi ndi awiriwo. 18 Pamene
ankadya pa tebulo Iye anati, "Zoonadi, ndikuwuzani kuti mmodzi wa inu
adzandipereka, mmodzi amene akudya ndi Ine."

19 Iwo anamva chisoni, ndipo mmodzi ndi mmodzi anati kwa Iye, "Kodi
ndine?"

[20] Iye anayankha kuti, "Ndi mmodzi mwa khumi ndi awirinu, amene
akusunsa buledi m'mbale pamodzi ndi Ine. [21] Mwana wa Munthu adzapita
monga momwe zinalembedwera za Iye. Koma tsoka kwa munthu amene
adzapereka Mwana wa Munthu! Kukanakhala bwino kwa iye akanapanda
kubadwa."
[22] Pamene ankadya, Yesu anatenga buledi, nayamika ndipo anamun-
yema nagawira ophunzira ake nanena kuti, "Tengani, ili ndi thupi langa."
[23] Kenaka anatenga chikho, nayamika nachipereka kwa iwo ndipo onse
anamweramo.
[24] Iye anawawuza kuti, "Awa ndi magazi anga a pangano amene
akhetsedwa chifukwa cha ambiri. [25] Zoonadi, ndikuwuzani kuti sin-
didzamwanso kuchokera ku chipatso cha mphesa mpaka tsikulo pamene
ndidzamwa chatsopano mu ufumu wa Mulungu."
[26] Atayimba nyimbo, anapita ku phiri la Olivi.

### *Yesu Aneneratu zakuti Petro Adzamukana*

[27] Yesu anati, "Nonse mudzandithawa, pakuti kwalembedwa:
" 'Kantha M'busa,
ndipo nkhosa zidzabalalika.'
[28] Koma ndikadzauka, ndidzatsogola kupita ku Galileya."
[29] Petro anati, "Ngakhale onse adzakuthaweni, ine sindidzatero."
[30] Yesu anayankha kuti, "Zoona ndikukuwuza kuti lero lino, usiku uno,
tambala asanalire kawiri, iweyo udzandikana katatu."
[31] Koma Petro ananenetsa kuti, "Ngakhale kutakhala kufa nanu, ine
sindidzakukanani." Ndipo ena onse ananena chimodzimodzi.

### *Mu Getsemani*

[32] Ndipo anapita ku malo otchedwa Getsemani, ndipo Yesu anati kwa
ophunzira ake, "Khalani pano pamene Ine ndi kupemphera." [33] Iye
anatenga Petro, Yakobo ndi Yohane, ndipo anayamba kumva chisoni
kwambiri ndi kuvutika mu mtima. [34] Iye anawawuza kuti, "Moyo wanga
wagwidwa ndi chisoni chofa nacho. Khalani pano ndipo musagone."
[35] Atapita patsogolo pang'ono, anagwa pansi ndi kupemphera kuti ngati
ndi kotheka oralo limupitirire. [36] Iye anati, "Abba, Atate, zinthu zonse
ndi zotheka ndi Inu. Chotsereni chikhochi. Komabe chitani zimene Inu
mukufuna, osati zimene Ine ndikufuna."
[37] Kenaka anabwerera kwa ophunzira ake ndipo anawapeza akugona,
Iye anati kwa Petro, "Simoni, kodi uli mtulo? Kodi simukanatha kukhala
maso kwa ora limodzi? [38] Khalani tcheru ndi kupemphera kuti musalowe
m'mayesero. Mzimu ukufuna, koma thupi ndi lofowoka."
[39] Kenakanso anachoka ndi kukapemphera chimodzimodzi. [40] Iye atab-
werera, anawapezanso akugona, chifukwa m'maso mwawo munadzaza
tulo. Iwo sanadziwe choti anene kwa Iye.
[41] Atabweranso kachitatu, anawafunsa kuti, "Kodi mukugonabe ndi
kupumula? Pakwana! Nthawi yafika. Taonani, Mwana wa Munthu
akuperekedwa m'manja mwa anthu ochimwa. [42] Nyamukani! Tiyeni
tizipita! Uyu wondipereka Ine wafika!"

### *Amugwira Yesu*

[43] Iye akuyankhulabe, Yudasi, mmodzi mwa khumi ndi awiriwo,
anatulukira. Anali ndi gulu la anthu litanyamula malupanga ndi zibonga,
otumidwa ndi akulu a ansembe, aphunzitsi amalamulo, ndi akuluakulu.

44 Tsopano womupereka anapangana chizindikiro ndi iwo kuti:
"Amene ndikapsompsone ndi iyeyo; mukamugwire ndi kumutenga ali
womangidwa." 45 Atapita kwa Yesu nthawi yomweyo, Yudasi anati,
"Aphunzitsi," ndipo anapsompsona. 46 Anthu anamugwira Yesu ndi
kumumanga. 47 Kenaka mmodzi wa iwo amene anayima pafupipo
anatulutsa lupanga lake nakhapa wantchito wa wamkulu wa ansembe,
n'kudula khutu lake.
48 Yesu anati, "Kodi Ine ndikutsogolera gulu lowukira, kuti mubwera ndi
malupanga ndi zibonga kudzandigwira? 49 Tsiku ndi tsiku ndinali ndi inu,
kuphunzitsa m'mabwalo a Nyumba ya Mulungu, koma inu simunandig-
wire. Koma malemba ayenera kukwaniritsidwa." 50 Pamenepo ophunzira
ake onse anathawa namusiya yekha.
51 Mnyamata wamng'ono amene anangofundira nsalu yokha, wopanda
chovala ankamutsatira Yesu. Atamugwira, 52 anathawa wamaliseche
kusiya nsalu yake m'mbuyo.

### *Yesu ku Bwalo la Milandu*

53 Anamutengera Yesu kwa mkulu wa ansembe, ndipo akulu a ansembe,
akuluakulu ndi aphunzitsi amalamulo anasonkhana pamodzi. 54 Petro
anamutsatira ali patali, mpaka ku bwalo la mkulu wa ansembe. Kumeneko
anakhala pansi ndi alonda namawotha moto.
55 Akulu a ansembe ndi onse olamulira a Ayuda ankafunafuna umboni
womutsutsa Yesu kuti amuphe, koma sanapeze wina uliwonse. 56 Ambiri
anamunenera Iye maumboni abodza, koma maumboni awo sanagwi-
rizane.
57 Kenaka ena anayimirira namunenera umboni wonama womutsutsa
Iye kunena kuti, 58 "Tamumva akunena kuti, 'Ndidzawononga Nyumba ya
Mulungu iyi yopangidwa ndi anthu ndipo m'masiku atatu ndidzamanga
ina, osati yopangidwa ndi munthu.' " 59 Ngakhale iwonso umboni wawo
sunagwirizane.
60 Kenaka mkulu wa ansembe anayimirira pakati pawo namufunsa
Yesu kuti, "Kodi suyankha? Kodi umboni uwu ndi wotani umene anthu
akukuchitira?" 61 Koma Yesu anakhala chete ndipo sanayankhe.
Mkulu wa ansembe anabwereza kumufunsa Iye kuti, "Kodi ndiwe
Khristu Mwana wa Wodalitsikayo?"
62 Yesu anati, "Ndine, ndipo mudzaona Mwana wa Munthu atakhala
kudzanja lamanja la Wamphamvuzonse ndipo akubwera m'mitambo ya
kumwamba."
63 Mkulu wa ansembe anang'amba zovala zaunsembe zake. Iye
anafunsa kuti, "Chifukwa chiyani tikufuna mboni zinanso? 64 Mwamva
mwanowo. Muganiza chiyani?"
Onse anavomereza kuti ndi woyenera imfa. 65 Kenaka ena anayamba
kumulavulira malovu; anamumanga m'maso, namumenya ndi zibakera
ndipo anati, "Nenera!" Ndipo asilikali anamutenga namumenya.

### *Petro Akana Yesu*

66 Petro ali chakumunsi kwa bwalo la milandu, mmodzi wa atsikana a
ntchito a mkulu wa ansembe anabwera. 67 Ataona Petro akuwotha moto,
anamuyang'anitsitsa.
Iye anati, "Iwenso unali pamodzi ndi Mnazareti, Yesu."
68 Koma iye anakana nati, "Sindikudziwa kapena kumvetsetsa zimene
ukuyankhula." Ndipo anachoka napita ku chipata.

69 Pamene mtsikana wantchitoyo anamuona iye, anatinso kwa iwo
amene anayimirira pomwepo, “Munthu uyu ndi mmodzi mwa iwo.”
70 Anakananso kachiwiri.
Patapita kanthawi pang’ono, amene anayimirira pafupi anati kwa Petro,
“Zoonadi ndiwe mmodzi wa iwo, pakuti ndiwe mu Galileya.”
71 Iye anayamba kudzitemberera, nalumbira kuti, “Sindimudziwa
munthu ameneyu.”
72 Nthawi yomweyo tambala analira kachiwiri. Pamenepo Petro
anakumbukira mawu amene Yesu ananena anamuwuza kuti, “Tambala
asanalire kawiri, iwe udzandikana katatu.” Ndipo iye anasweka mtima
nayamba kulira.

# 15

*Yesu ku Bwalo la Pilato*

1 Mmamawa, akulu a ansembe pamodzi ndi akuluakulu, aphunzitsi
amalamulo ndi olamulira onse anamanga fundo. Anamumanga Yesu,
namutenga ndi kukamupereka kwa Pilato.
2 Pilato anafunsa kuti, “Kodi Iwe ndi Mfumu ya Ayuda?”
Yesu anayankha kuti, “Mwatero ndinu.”
3 Akulu a ansembe anamunenera zinthu zambiri.
4 Ndipo Pilato
anamufunsanso Iye kuti, “Kodi Iwe suyankhapo kanthu? Tamva zinthu
zambiri akukunenerazi.”
5 Koma Yesu sanayankhebe, ndipo Pilato anadabwa.
6 Pa nthawi ya Phwando, panali chizolowezi chomasula munthu
wam’ndende amene anthu amupempha.
7 Munthu wotchedwa Baraba
anali m’ndende pamodzi ndi anthu owukira amene anapha anthu pa
nthawi ya chipolowe.
8 Gulu la anthu linabwera kwa Pilato ndi kumufunsa
kuti awachitire zimene amachita nthawi zonse.
9 “Kodi mukufuna kuti ndikumasulireni mfumu ya Ayuda?” Pilato
anafunsa,
10 podziwa kuti akulu a ansembe anamupereka Yesu kwa iye
chifukwa cha nsanje.
11 Koma akulu a ansembe anasonkhezera anthu kuti
Pilato amasule Baraba m’malo mwa Yesu.
12 Pilato anawafunsa kuti, “Kodi nanga ndichite chiyani ndi uyu amene
mukumutcha mfumu ya Ayuda?”
13 Anafuwula kuti, “Mpachikeni!”
14 Pilato anafunsa kuti, “Chifukwa chiyani? Wapalamula mlandu
wotani?”
Koma anafuwula kwambiri, “Mpachikeni!”
15 Pilato pofuna kuwakondweretsa anthuwo, anawamasulira Baraba.
Analamula kuti Yesu akwapulidwe mwankhanza, ndipo anamupereka kuti
akapachikidwe.

*Chipongwe cha Asilikali*

16 Asilikali anamutenga Yesu ndi kupita naye m’kati mwa nyumba
yaufumu (dera lokhalako asilikali a mfumu) ndipo anasonkhanitsa gulu
lonse la asilikali.
17 Anamuveka Iye mwinjiro wofiira, kenaka analuka
chipewa cha minga ndi kuyika pa mutu pake.
18 Ndipo anayamba
kunena kwa Iye kuti, “Ulemu kwa inu Mfumu ya Ayuda!”
19 Ndipo
anamugogoda pa mutu mobwerezabwereza ndi ndodo ndi kumulavulira.
Anamugwadira ndi kumulambira Iye.
20 Ndipo anamuchita chipongwe,

anamuvula mwinjiro wofiira uja ndi kumuveka zovala zake. Kenaka
anamutenga kuti akamupachike.

### *Yesu Apachikidwa pa Mtanda*

21 Munthu wina ochokera ku Kurene, Simoni, abambo a Alekisanda
ndi Rufasi amadutsa kuchokera ku dziko la kwawo, ndipo anamuwum-
iriza kuti anyamule mtanda. 22 Anafika naye Yesu pa malo otchedwa
Gologota (kutanthauza kuti, malo a bade) 23 Kenaka anamupatsa Iye
vinyo wosakaniza ndi mure, koma Iye sanamwe. 24 Ndipo anamupachika
Iye. Anachita maere ogawana zovala zake kuti aone chimene aliyense
angatenge.

25 Linali ora lachitatu mmawa pamene anamupachika Yesu.
26 Chikwangwani cholembedwapo mlandu wake chinali choti: MFUMU
YA AYUDA. 27 Achifwamba awiri anapachikidwanso pamodzi ndi Iye,
wina kumanja kwake ndi wina kumanzere kwake. 28 (Ndipo malemba
anakwaniritsidwa amene amati, “Iye anayikidwa m’gulu la anthu oyipa).”
29 Amene amadutsa pafupi anamunenera mawu amwano, akupukusa
mitu yawo ndi kuti, “Haa! Iwe amene udzawononga Nyumba ya Mulungu
ndi kuyimanganso masiku atatu, 30 tsika kuchoka pa mtandapo ndipo
udzipulumutse wekha!”

31 Chimodzimodzinso akulu a ansembe ndi aphunzitsi amalamulo
anamunyoza Iye pakati pawo. Iwo anati, “Anapulumutsa ena, koma
sangathe kudzipulumutsa yekha! 32 Musiyeni Khristu, Mfumu ya Aisraeli,
atsike tsopano kuchoka pa mtanda, kuti ife tione ndi kukhulupirira.”
Iwonso amene anapachikidwa naye pamodzi anamulalatira.

### *Imfa ya Yesu*

33 Pa ora lachisanu ndi chimodzi masana mdima unabwera pa dziko
lonse mpaka pa ora lachisanu ndi chinayi masana. 34 Pa ora lachisanu
ndi chinayi Yesu analira mofuwula kuti, “Eloi, Eloi, lama sabakitani?”
Kutanthauza kuti, “Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji
Ine?”

35 Ena amene anali pafupi atamva izi anati, “Tamverani, akuyitana
Eliya.”

36 Munthu wina anathamanga, natenga chinkhupule atachiviyika mu
vinyo wosasa, anachizika ku mtengo, ndi kumupatsa Yesu kuti amwe.
Munthuyo anati, “Musiyeni yekha tsopano. Tiyeni tione ngati Eliya
angabwere kudzamutsitsa.”

37 Ndi mawu ofuwula, Yesu anapuma komaliza.

38 Chinsalu chotchinga cha m’Nyumba ya Mulungu chinang’ambika
pakati kuyambira pamwamba mpaka pansi. 39 Ndipo Kenturiyo, amene
anayima patsogolo pa Yesu, atamva kulira kwake ndi kuona mmene
anafera anati, “Zoonadi, uyu anali Mwana wa Mulungu.”

40 Amayi ena anali patali kuonerera. Pakati pawo panali Mariya
Magadalena, Mariya amayi a Yakobo wamng’ono ndi Yose ndi Salome.
41 Amayi awa ankamutsatira Iye mu Galileya ndi kumutumikira Iye pa
zosowa zake. Amayi enanso ambiri amene anabwera naye ku Yerusalemu
analinso pomwepo.

### *Yesu Ayikidwa M’manda*

42 Linali Tsiku Lokonzekera (kunena kuti, tsiku lomwe limatsatizana
ndi Sabata). Choncho madzulo atayandikira, 43 Yosefe wa ku Ari-
mateyu, mkulu wolamulira odziwika bwino, amene amadikirira ufumu
wa Mulungu, anapita kwa Pilato molimba mtima ndi kukapempha
mtembo wa Yesu. 44 Pilato anadabwa pakumva kuti anali atamwalira
kale. Anayitana Kenturiyo, namufunsa ngati Yesu anali atamwalira kale.
45 Atawuzidwa ndi Kenturiyo kuti zinali motero, anapereka mtembowo
kwa Yosefe. 46 Choncho Yosefe anagula nsalu yabafuta, natsitsa thupi,
ndipo analikulunga m'nsalu, naliyika m'manda amene anawagoba pa
mwala. Kenaka anagubuduza mwala umene anatseka nawo mandawo.
47 Mariya Magadalena ndi Mariya amayi a Yose anaona kumene ana-
muyika Yesu.

# 16

*Kuuka kwa Yesu*

1 Litapita tsiku la Sabata, Mariya Magadalena, ndi amayi ake a Yakobo,
ndi Salome anagula zonunkhiritsa ndi cholinga chakuti apite akadzoze
thupi la Yesu. 2 Mmamawa, tsiku loyamba la Sabata, dzuwa litangotuluka
kumene, anali pa ulendo wopita ku manda 3 ndipo anafunsana wina ndi
mnzake kuti, "Kodi akatikugudubuzira mwala pa khomo la manda ndani?"
4 Koma atakweza maso awo, anaona kuti mwala umene unali waukulu
kwambiri wagubuduzidwa kale. 5 Atalowa m'manda, anaona mnyamata
atavala mwinjiro woyera atakhala ku mbali ya kumanja, ndipo iwo
anachita mantha.
6 Iye anati, "Musaope. Kodi mukufuna Yesu wa ku Nazareti, amene
anapachikidwa? Wauka! Sali muno. Onani malo amene anamu-
gonekapo. 7 Koma pitani, kawuzeni ophunzira ake ndi Petro kuti, 'Iye
watsogola kupita ku Galileya. Kumeneko mukamuona Iye monga momwe
anakuwuzirani.' "
8 Akunjenjemera ndi kudabwa, amayiwo anatuluka ndipo anathawa ku
mandako. Sananene china chilichonse kwa aliyense, chifukwa anachita
mantha.

*[Mipukutu yoyambirira ndi maumboni akale mulibe vesi 9 mpaka 20.]*

*Yesu Aonekera kwa Mariya Magadalena*

9 Yesu atauka kwa akufa mmawa pa tsiku loyamba la Sabata, anayamba
kuonekera kwa Mariya Magadalena, amene anatulutsa mwa iye ziwanda
zisanu ndi ziwiri. 10 Iye anapita ndi kukawawuza amene anali ndi Yesu,
amene ankakhuza maliro ndi kulira. 11 Atamva kuti Yesu ali moyo ndikuti
amuona, iwo sanakhulupirire.

*Yesu Aonekera kwa Ophunzira Awiri*

12 Zitatha izi Yesu anaonekera m'maonekedwe ena kwa awiri a iwo
amene anali ku dera la ku mudzi. 13 Iwo anabwerera ndi kudzawawuza
enawo; koma iwo sanakhulupirirebe.

*Yesu Ayankhula kwa Ophunzira Khumi ndi Mmodzi*

14 Pambuyo pake Yesu anaonekera kwa khumi ndi mmodziwo pamene
ankadya; anawadzudzula chifukwa chopanda chikhulupiriro ndi kukanit-
sitsa kwawo kuti akhulupirire amene anamuona Iye atauka.
15 Anati kwa iwo, "Pitani m'dziko lonse lapansi ndipo mukala-
likire Uthenga Wabwino kwa zolengedwa zonse. 16 Aliyense amene

akakhulupirire nabatizidwa adzapulumuka, koma amene sakakhulupirira
adzalangidwa. [17] Tsono zizindikiro izi zidzawatsata amene adza-
khulupirira: M'dzina langa adzatulutsa ziwanda; adzayankhula malilime
atsopano; [18] adzanyamula njoka ndi manja awo; ndipo pamene adzamwa
mankhwala akupha, sadzawapweteka n'pang'onong'ono pomwe; adza-
sanjika manja awo pa anthu odwala ndipo odwalawo adzachira."

### *Yesu Apita Kumwamba*

[19] Ambuye Yesu atatha kuyankhulana nawo, anatengedwa kupita
kumwamba ndipo anakhala kudzanja lamanja la Mulungu. [20] Pamenepo
ophunzira aja anapita ndi kukalalikira ponseponse, ndipo Ambuye anag-
wira nawo ntchito pamodzi, ndipo anatsimikizira mawuwo ndi zizindikiro
zimene ankachita.

# UTHENGA WABWINO WA YESU KHRISTU WOLEMBEDWA NDI LUKA

## *Mawu Oyamba*

1 Ambiri anayesa kufotokoza nkhani ya zimene zinakwaniritsidwa
pakati pathu, 2 monga mmene zinaperekedwera kwa ife ndi iwo amene
anaona poyambirira ndi atumiki a mawu. 3 Popeza inenso ndafufuza
mosamalitsa chilichonse kuyambira pachiyambi, zandikomera kukulem-
berani mwatsatanetsatane inu wolemekezeka Tiofilo, 4 kuti mudziwe
bwinobwino zoona za zinthu zimene mwaphunzitsidwa.

## *Aneneratu za Kubadwa kwa Yohane M'batizi*

5 M'masiku a Herode, mfumu ya Yudeya, kunali wansembe dzina lake
Zakariya wa gulu la ansembe la Abiya; mkazi wake Elizabeti analinso
wa fuko la Aaroni. 6 Onse awiri anali olungama pamaso pa Mulungu,
ndipo amasunga malamulo ndi malangizo onse a Ambuye osalakwa konse.
7 Koma analibe ana chifukwa Elizabeti anali wosabereka; ndipo onse anali
okalamba.

8 Nthawi yogwira ntchito yotumikira ansembe a gulu la Zekariya,
Zekariya ankatumikira ngati wansembe pamaso pa Mulungu, 9 Zakariyayo
anasankhidwa mwa maere, monga mwa mwambo wa unsembe, kupita
m'Nyumba ya Ambuye kukafukiza lubani. 10 Ndipo nthawi yofukiza
lubani itafika, gulu lonse lopembedza linkapemphera kunja.

11 Kenaka mngelo wa Ambuye anaonekera kwa iye, atayimirira ku
dzanja lamanja la guwa lofukizira. 12 Zakariya ataona mngeloyo, anadzidz-
imuka ndipo anagwidwa ndi mantha. 13 Koma mngeloyo anati kwa
iye: "Usachite mantha, Zakariya; pemphero lako lamveka. Mkazi wako
Elizabeti adzakuberekera iwe mwana wamwamuna ndipo udzamutche
dzina loti Yohane. 14 Ndipo adzakhala chimwemwe ndi chisangalalo
kwa iwe, ndipo ambiri adzasangalala chifukwa cha kubadwa kwake,
15 chifukwa adzakhala wamkulu pamaso pa Ambuye. Iye sadzamwa vinyo
kapena chakumwa choledzeretsa, ndipo adzazadzidwa ndi Mzimu Woyera
kuyambira pa kubadwa. 16 Iye adzabweretsanso Aisraeli ambiri kwa
Ambuye Mulungu wawo. 17 Ndipo iye adzabwera Ambuye asanabwere
mu mzimu ndi mphamvu ya Eliya. Adzatembenuzira mitima ya abambo
kwa ana awo ndi osamvera ku nzeru ya olungama, kuthandiza anthu kuti
akonzekere kubwera kwa Ambuye."

18 Zakariya anamufunsa mngeloyo kuti, "Kodi ndingatsimikize bwanji
zimenezi? Ine ndine wokalamba ndipo mkazi wanga ali ndi zaka zambiri."

19 Mngeloyo anayankha kuti, "Ine ndine Gabrieli. Ndimayima pamaso
pa Mulungu, ndipo ndatumidwa kwa iwe kudzakuwuza uthenga wab-
winowu. 20 Ndipo kuyambira tsopano sudzatha kuyankhula kufikira izi zi-
tachitika chifukwa sunakhulupirire mawu awa, amene adzakwaniritsidwe
pa nthawi yake yoyenera."

21 Pa nthawiyi, anthu ankadikira Zakariya ndipo anadabwa chifukwa
anatenga nthawi yayitali ali m'Nyumba ya Mulungu. 22 Atatuluka
sanathe kuyankhulana nawo. Anazindikira kuti anaona masomphenya

m'Nyumbamo, chifukwa ankasonyeza zizindikiro kwa iwo koma sankatha
kuyankhula.
23 Nthawi yake yotumikira itatha, anabwerera kwawo. 24 Zitatha
izi, mkazi wake Elizabeti anakhala ndi pakati ndipo anadzibisa kwa
miyezi isanu. 25 Iye anati, "Ambuye wandichitira izi, kuti m'masiku ano
wandionetsera kukoma mtima kwake ndi kuchotsa manyazi anga pakati
pa anthu."

*Aneneratu za Kubadwa kwa Yesu*

26 Mwezi wachisanu ndi chimodzi, Mulungu anatuma mngelo Gabrieli
ku Nazareti, mudzi wa ku Galileya, 27 kwa namwali wopalidwa ub-
wenzi ndi Yosefe, wa fuko la Davide. Dzina la namwaliyo linali
Mariya. 28 Mngeloyo anafika kwa iye nati, "Moni, inu amene Ambuye
wakukomerani mtima kwambiri! Ambuye ali ndi inu."
29 Mariya anavutika kwambiri ndi mawu awa ndipo anadabwa ndi
kulonjera kotere. 30 Koma mngeloyo anati kwa iye, "Usachite mantha
Mariya, pakuti wapeza chisomo pamaso Mulungu. 31 Udzakhala woyem-
bekezera ndipo udzabala mwana wamwamuna ndipo udzamupatse dzina
loti Yesu. 32 Iye adzakhala wamkulu ndipo adzatchedwa Mwana wa
Wammwambamwamba. Ambuye Mulungu adzamupatsa Iye mpando
waufumu wa abambo ake Davide, 33 ndipo adzalamulira pa nyumba ya
Yakobo ku nthawi zonse; ufumu wake sudzatha."
34 Mariya anafunsa mngeloyo kuti, "Izi zingatheke bwanji popeza ine
sindidziwa mwamuna?"
35 Mngelo anayankha kuti, "Mzimu Woyera adzabwera pa iwe ndipo
mphamvu ya Wammwambamwamba idzakuphimba, ndipo Woyerayo
amene adzabadwe adzatchedwa Mwana wa Mulungu. 36 Ngakhale
Elizabeti m'bale wako adzakhala ndi mwana mu ukalamba wake ndipo iye
amene amati ndi wosabereka, uno mwezi wake wachisanu ndi chimodzi.
37 Pakuti palibe chinthu chosatheka ndi Mulungu."
38 Mariya anayankha kuti, "Ine ndine mtumiki wa Ambuye. Zikhale kwa
ine monga mwanenera."

*Mariya Acheza kwa Elizabeti*

39 Nthawi imeneyo anakonzeka ndipo anapita mofulumira ku mudzi
wa ku mapiri a dziko la Yudeya, 40 kumene anakalowa m'nyumba ya
Zakariya nalonjera Elizabeti. 41 Elizabeti atamva moni wa Mariya, mwana
anatakataka m'mimba mwake, ndipo Elizabeti anadzazidwa ndi Mzimu
Woyera. 42 Anafuwula ndi mawu akulu kuti, "Ndiwe wodala pakati pa
akazi, ndipo ndi wodala mwana amene udzabereke! 43 Koma n'chifukwa
chiyani andikomera mtima kuti amayi a Ambuye anga abwere kwa
ine? 44 Nthawi yomwe ndinamva mawu akulonjera kwanu, mwana
anatakataka m'mimba mwanga chifukwa cha chimwemwe. 45 Wodala
iye amene wakhulupirira kuti chimene Ambuye wanena kwa iye chidza-
kwaniritsidwa!"

*Nyimbo ya Mariya*

46 Ndipo Mariya anati:
"Moyo wanga ulemekeza Ambuye.
47 Ndipo mzimu wanga ukondwera mwa Mulungu Mpulumutsi wanga,
48 pakuti wakumbukira
kudzichepetsa kwa mtumiki wake.
Kuyambira tsopano mibado yonse idzanditcha wodala,

49 pakuti Wamkuluyo wandichitira ine zinthu zazikulu,
dzina lake ndi loyera.
50 Chifundo chake chifikira kwa iwo amene amuopa Iye
kufikira mibadomibado.
51 Iye wachita zamphamvu ndi dzanja lake;
Iye anabalalitsa iwo amene ali onyada m'maganizo awo.
52 Iye anachotsa olamulira pa mipando yawo yaufumu,
koma wakweza odzichepetsa.
53 Iye wakhutitsa a njala ndi zinthu zabwino
koma anachotsa olemera wopanda kanthu.
54 Iye anathandiza mtumiki wake Israeli,
pokumbukira chifundo chake.
55 Kwa Abrahamu ndi zidzukulu zake ku nthawi zonse
monga ananena kwa makolo athu."
56 Mariya anakhala ndi Elizabeti pafupifupi miyezi itatu ndipo kenaka
anabwerera kwawo.

### *Kubadwa kwa Yohane M'batizi*

57 Itakwana nthawi yoti Elizabeti abereke, anabereka mwana wamwa-
muna. 58 Anansi ndi abale ake anamva kuti Ambuye anamuchitira
chifundo chachikulu ndipo anakondwera naye pamodzi.
59 Pa tsiku lachisanu ndi chitatu anabwera ndi mwana kuti adzachitidwe
mdulidwe, ndipo anafuna kumupatsa dzina la abambo ake Zakariya,
60 koma amayi ake anayankhula nati, "Ayi, atchulidwe kuti Yohane."
61 Iwo anati kwa iye, "Palibe mmodzi mwa abale ake amene ali ndi dzina
limeneli."
62 Pamenepo anapanga zizindikiro kwa abambo ake kuti adziwe dzina
limene akanakonda kumutcha mwanayo. 63 Iye anapempha poti alem-
bepo, ndipo chodabwitsa kwa aliyense analemba kuti, "Dzina lake ndi
Yohane." 64 Nthawi yomweyo pakamwa pake panatsekuka ndi lilime lake
linamasuka ndipo anayamba kuyankhula, nayamika Mulungu. 65 Anansi
onse anachita mantha kwambiri, ndipo ku madera onse a kumapiri a
Yudeya, anthu anayankhula zinthu zonsezi. 66 Aliyense amene anamva
izi anadabwa nazo nafunsa kuti, "Kodi mwana uyu adzakhala wotani?"
Pakuti dzanja la Ambuye lili pa iye.

### *Nyimbo ya Zakariya*

67 Abambo ake, Zakariya, anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo
ananenera kuti,
68 "Alemekezeke Ambuye, Mulungu wa Israeli
chifukwa wabwera ndi kuwombola anthu ake.
69 Iye wakweza nyanga yachipulumutso kwa ife
mu nyumba ya mtumiki wake Davide.
70 (Monga mmene ananenera kudzera mwa aneneri oyera),
71 chipulumutso kuchoka kwa adani athu
ndi kuchoka m'dzanja la onse otida,
72 kuonetsa chifundo kwa makolo athu
ndi kukumbukira pangano lake loyera,
73 lumbiro limene analumbira kwa kholo lathu Abrahamu:
74 kutilanditsa ife m'dzanja la adani athu,
ndi kutipanga ife timutumikire Iye mopanda mantha,
75 m'chiyero ndi m'chilungamo masiku athu onse.

76 “Ndipo iwe mwana wanga udzatchedwa mneneri wa Wammwambamwamba;
pakuti udzapita patsogolo pa Ambuye kukonza njira yake,
77 kupatsa anthu ake chidziwitso cha chipulumutso
kudzera mwa chikhulululukiro cha machimo awo,
78 chifukwa cha chifundo chachikulu cha Mulungu wathu,
ndipo kuwala kwa dzuwa kudzafikira ife kuchokera kumwamba,
79 kuwalira iwo okhala mu mdima
ndi mu mthunzi wa imfa,
kutsogolera mapazi athu mu njira yamtendere.”

80 Ndipo mwanayo anakula nakhala wamphamvu mu mzimu; ndipo
anakhala ku chipululu mpaka pamene anaonekera poyera mu Israeli.

# 2

*Kubadwa kwa Yesu*

1 M’masiku amenewo Kaisara Augusto anapereka lamulo kuti kalembera
achitike m’dziko lonse la Aroma. 2 (Uyu ndi kalembera woyamba amene
anachitika pamene Kureniyo anali bwanamkubwa wa Siriya). 3 Ndipo
aliyense anapita ku mzinda wa kwawo kukalembetsa.

4 Choncho Yosefe anachoka ku Nazareti ku Galileya kupita ku Yudeya,
ku Betelehemu ku mudzi wa Davide, chifukwa anali wa banja ndi
fuko la Davide. 5 Iye anapita kumeneko kukalembetsa pamodzi ndi
Mariya, amene anapalana naye ubwenzi kuti akwatirane ndipo anali
woyembekezera. 6 Ali kumeneko, nthawi inakwana yakuti mwana
abadwe, 7 ndipo anabereka mwana wake woyamba, wamwamuna. Iye
anamukulunga m’nsalu ndi kumuyika modyera ng’ombe, chifukwa ku-
nalibe malo m’nyumba ya alendo.

*Abusa ndi Angelo*

8 Ndipo kunali abusa amene amakhala ku dera lomwelo, kuyang’anira
ziweto zawo usiku. 9 Mngelo wa Ambuye anaonekera kwa iwo ndipo
ulemerero wa Ambuye unawala mowazungulira. Iwo anachita man-
tha. 10 Koma mngeloyo anawawuza kuti, “Musachite mantha. Ine
ndakubweretserani Uthenga Wabwino wachimwemwe chachikulu umene
udzakhala wa anthu onse. 11 Lero m’mudzi wa Davide wakubwadwirani
Mpulumutsi; Iye ndi Khristu Ambuye. 12 Ichi chidzakhala chizindikiro kwa
inu: mukapeza mwana wakhanda wokutidwa ndi nsalu atagona modyera
ng’ombe.”

13 Mwadzidzidzi gulu lalikulu la angelo linaonekera pamodzi ndi
mngeloyo, kuyamika Mulungu ndi kumati,

14 “Ulemerero kwa Mulungu mmwambamwamba,
ndi mtendere kwa anthu pa dziko lapansi amene Iye akondwera nawo.”

15 Angelowo atabwerera kumwamba, abusawo anati kwa wina ndi
mnzake, “Tiyeni ku Betelehemu tikaone zinthu zomwe zachitika, zimene
Ambuye atiwuza ife.”

16 Ndipo iwo anafulumira nyamuka nakapeza Mariya ndi Yosefe ndi
mwana wakhanda, amene anagona modyera ng’ombe. 17 Pamene ana-
muona Iye, iwo anafotokoza zomwe anawuzidwa za mwanayo, 18 ndipo
onse amene anamva zimene abusawa ananena anadabwa. 19 Koma
Mariya anasunga zonsezi mu mtima mwake ndi kumazilingalira. 20 Abusa

anabwerera, akulemekeza ndi kuyamika Mulungu chifukwa cha zonse anazimva ndi kuziona, zomwe zinali monga anawuzidwira ndi angelo aja.

### *Yesu Aperekedwa m'Nyumba ya Mulungu*

21 Pa tsiku lachisanu ndi chitatu, tsiku loti amuchite mdulidwe anamutcha Yesu, dzina limene mngelo anamupatsa asanabadwe.
22 Nthawi yoyeretsedwa kwawo itatha, monga mwa lamulo la Mose,
Yosefe ndi Mariya anapita naye ku Yerusalemu kukamupereka kwa
Ambuye. 23 (Monga mmene zinalembedwera mu lamulo la Ambuye kuti,
"Muzikapereka kwa Ambuye mwana aliyense wamwamuna woyamba
kubadwa"), 24 ndi kupereka nsembe posunga zimene zinanenedwa mulamulo la Ambuye: "Njiwa ziwiri kapena mawunda ankhunda awiri."
25 Ndipo taonani, mu Yerusalemu munali munthu wotchedwa Simeoni,
amene anali wolungama ndi wodzipereka. Iye ankadikira chitonthozo cha
Israeli, ndipo Mzimu Woyera anali pa iye. 26 Mzimu Woyera anamuwululira kuti sadzafa asanaone Khristu wa Ambuye. 27 Motsogozedwa ndi
Mzimu Woyera, iye anapita ku bwalo la Nyumba ya Mulungu. Makolo ake
a Yesu atabwera naye kuti achite naye mwambo malingana ndi malamulo,
28 Simeoni anamunyamula m'manja mwake nayamika Mulungu, nati:
29 "Ambuye waulamuliro, monga munalonjeza,
tsopano lolani kuti mtumiki wanu apite mu mtendere.
30 Pakuti maso anga aona chipulumutso chanu,
31 chimene Inu munakonza pamaso pa anthu onse,
32 kuwala kowunikira anthu a mitundu ina
ndi kwa ulemerero kwa anthu anu Aisraeli."
33 Abambo ndi amayi a Mwanayo anadabwa chifukwa cha zimene
zinanenedwa za Iye. 34 Kenaka Simeoni anawadalitsa ndipo anati
kwa Mariya amayi ake: "Mwana uyu wakonzedwa kukhala kugwa
ndi kudzuka kwa ambiri mu Israeli, ndi kukhala chizindikiro chimene
adzayankhula motsutsana nacho, 35 kotero kuti malingaliro a mitima ya
ambiri adzawululidwa. Ndipo lupanga lidzabaya moyo wakonso."
36 Panalinso mneneri wamkazi, dzina lake Ana, mwana wa Fanuelo,
wa fuko la Aseri. Anali wokalamba kwambiri; anakhala ndi mwamuna
wake zaka zisanu ndi ziwiri atakwatiwa, 37 ndipo kenaka anakhala
wamasiye mpaka pamene anali ndi zaka 84. Iye sanachoke m'Nyumba
ya Mulungu koma ankapembedza usiku ndi usana, kusala kudya ndi
kupemphera. 38 Pa nthawiyo pamene ankapita kwa iwo, iye anayamika
Mulungu ndi kuyankhula za Mwanayo kwa onse amene ankayembekezera
chipulumutso cha Yerusalemu.
39 Yosefe ndi Mariya atachita zonse zimene zinkafunikira ndi lamulo
la Ambuye, anabwerera ku Galileya ku mudzi wa Nazareti. 40 Ndipo
Mwanayo anakula nakhala wamphamvu; Iye anadzazidwa ndi nzeru,
ndipo chisomo cha Mulungu chinali pa Iye.

### *Yesu m'Nyumba ya Mulungu*

41 Chaka chilichonse makolo ake ankapita ku Yerusalemu ku phwando
la Paska. 42 Iye ali ndi zaka khumi ndi ziwiri, anapita ku phwando, monga
mwa mwambo. 43 Phwando litatha, pamene makolo ake ankabwerera
kwawo, mnyamata Yesu anatsalira ku Yerusalemu, koma iwo sanadziwe
zimenezi. 44 Poganiza kuti anali nawo m'gulu lawo, anayenda tsiku
limodzi. Kenaka anayamba kumufunafuna pakati pa abale awo ndi anzawo. 45 Atalephera kumupeza, anabwerera ku Yerusalemu kukamufuna.

46 Patatha masiku atatu anamupeza ali m'bwalo la Nyumba ya Mulungu,
atakhala pakati pa aphunzitsi, akumvetsera ndi kuwafunsa mafunso.
47 Aliyense amene anamumva Iye anadabwa ndi chidziwitso chake ndi
mayankho ake. 48 Makolo ake atamuona, anadabwa. Amayi ake anati kwa
Iye, "Mwanawe, watichitira zimenezi chifukwa chiyani? Abambo ako ndi
ine takhala tili ndi nkhawa kukufunafuna Iwe."

49 Iye anawafunsa kuti, "N'chifukwa chiyani mumandifunafuna? Kodi
simukudziwa kuti ndikuyenera kukhala m'nyumba ya Atate anga?"
50 Koma iwo sanazindikire chomwe Iye amatanthauza.

51 Kenaka anapita nawo ku Nazareti ndipo anawamvera iwo. Koma
amayi ake anasunga zinthu zonsezi mu mtima mwawo.

52 Ndipo Yesu anakula mu nzeru, msinkhu ndi chisomo cha Mulungu
ndi anthu.

# 3

### *Yohane M'batizi Akonza Njira*

1 M'chaka cha 15 mu ulamuliro wa Tiberiyo Kaisara, Pontiyo Pilato
ali bwanamkubwa wa Yudeya, Herode ankalamulira ku Galileya, m'bale
wake Filipo ankalamulira ku Iturea ndi ku dera la Trakoniti, ndipo
Lusaniyo ankalamulira ku Abilene. 2 Inalinso nthawi ya mkulu wa
ansembe wa Anasi ndi Kayafa, pamene mawu a Mulungu anabwera
kwa Yohane mwana wa Zakariya m'chipululu. 3 Iye anapita ku dziko
lonse lozungulira mtsinje wa Yorodani, nalalikira ubatizo wa kulapa ndi
kukhululukidwa kwa machimo. 4 Monga analembera m'buku la Yesaya
mneneri kuti:

"Mawu a wofuwula m'chipululu,
konzani njira ya Ambuye,
wongolani njira zake.
5 Chigwa chilichonse chidzadzazidwa
ndipo phiri lililonse ndi mtunda uliwonse zidzasalazidwa,
misewu yokhotakhota idzawongoledwa,
ndi njira zosasalala zidzasalazidwa.
6 Ndipo anthu onse adzaona chipulumutso cha Mulungu."

7 Yohane anati kwa magulu a anthu amene amabwera kudzabatizidwa
ndi iye, "Ana anjoka inu! Anakuchenjezani ndani kuti muthawe mkwiyo
umene ukubwera? 8 Onetsani zipatso zakutembenuka mtima, ndipo
musamanene mwa inu nokha kuti, 'Tili nalo kholo lathu Abrahamu,'
pakuti ndikuwuzani kuti kuchokera ku miyala iyi, Mulungu akhoza ku-
muwutsira Abrahamuyo ana. 9 Nkhwangwa ili kale pa muzu wamitengo,
ndipo mtengo uliwonse umene subala chipatso chabwino udzadulidwa ndi
kuponyedwa pa moto."

10 Gulu la anthuwo linafunsa kuti, "Nanga tsono tichite chiyani?"

11 Yohane anayankha kuti, "Munthu amene ali ndi malaya awiri apat-
seko amene alibe, ndi amene ali ndi chakudya achitenso chimodzimodzi."

12 Amisonkho nawonso anabwera kudzabatizidwa. Iwo anafunsa kuti,
"Aphunzitsi, ife tichite chiyani?"

13 Iye anawawuza kuti, "Musalandire moposa zimene muyenera."
14 Kenaka asilikali ena anamufunsa kuti, "Nanga ife tichite chiyani?"

Iye anayankha kuti, "Musamalande ndalama moopseza ndipo
musamanamizire anthu, khutitsidwani ndi malipiro anu."

15 Anthu ankadikira ndi chiyembekezo ndipo ankasinkhasinkha
m'mitima mwawo kuti mwina Yohane n'kukhala Khristu. 16 Yohane
anayankha onse kuti, "Ine ndikubatizani ndi madzi. Koma wina
wondiposa ine mphamvu adzabwera amene sindili woyenera kumasula
lamba wa nsapato zake. Iyeyu adzakubatizani inu ndi Mzimu Woyera
ndi moto. 17 M'dzanja lake muli chopetera kuti ayeretse powomberapo
tirigu ndi kusonkhanitsa tirigu ndipo adzatentha zotsalira zonse ndi moto
wosazimitsika." 18 Ndipo ndi mawu ena ambiri, Yohane anawachenjeza
anthu ndi kuwalalikira Uthenga Wabwino.
19 Koma pamene Yohane anadzudzula Herode wolamulirayo chifukwa
chokwatira Herodia, mkazi wa m'bale wake, ndi zoyipa zina zonse
anazichita, 20 Herode anawonjezanso choyipa ichi pa zonsezo: Anatsekera
Yohane m'ndende.

### *Ubatizo wa Yesu*

21 Pamene anthu onse ankabatizidwa, Yesu anabatizidwanso. Ndipo
akupemphera, kumwamba kunatsekuka. 22 Mzimu Woyera anatsika
pa Iye mumaonekedwe a nkhunda ndipo mawu anamveka kuchokera
kumwamba: "Iwe ndiwe Mwana wanga wokondedwa; ndimakondwera
nawe."

### *Makolo a Yesu*

23 Ndipo Yesu anali ndi zaka makumi atatu pamene anayamba ntchito
yake. Monga mmene anthu ankaganizira, Iyeyo anali mwana wa Yosefe,

mwana wa Heli, 24 mwana wa Matate,
mwana wa Levi, mwana wa Meliki,
mwana wa Yaneyi, mwana wa Yosefe
25 mwana wa Matati, mwana wa Amosi,
mwana wa Naomi, mwana wa Esli,
mwana wa Nagai, 26 mwana wa Maati,
mwana wa Matatiyo, mwana wa Simeoni,
mwana wa Yosefe, mwana wa Yoda
27 mwana wa Yohanani, mwana wa Resa,
mwana wa Zerubabeli, mwana wa Salatieli,
mwana wa Neri, 28 mwana wa Meliki,
mwana wa Adi, mwana wa Kosamu,
mwana wa Elmadama, mwana wa Ere,
29 mwana wa Jose, mwana wa Eliezara,
mwana wa Yorimu, mwana wa Matati,
mwana wa Levi, 30 mwana wa Simeoni,
mwana wa Yuda, mwana wa Yosefe,
mwana wa Yonamu, mwana wa Eliakimu,
31 mwana wa Meleya, mwana wa Mena,
mwana wa Matata, mwana wa Natani,
mwana wa Davide, 32 mwana wa Yese,
mwana wa Obedi, mwana wa Bowazi,
mwana wa Salimoni, mwana wa Naasoni,
33 mwana wa Aminadabu, mwana wa Arni,
mwana wa Hezronu, mwana wa Perezi,
mwana wa Yuda, 34 mwana wa Yakobo,
mwana wa Isake, mwana wa Abrahamu,
mwana wa Tera, mwana wa Nakoro,
35 mwana wa Serugi, mwana wa Reu,

mwana wa Pelegi, mwana wa Eberi,
mwana wa Sela, 36 mwana wa Kainane,
mwana wa Arfaksadi, mwana wa Semu,
mwana wa Nowa, mwana wa Lameki,
37 mwana wa Metusela, mwana wa Enoki,
mwana wa Yaredi mwana wa Malaleeli,
mwana wa Kainane, 38 mwana wa Enosi,
mwana wa Seti,
mwana wa Adamu, mwana wa Mulungu.

# 4

*Kuyesedwa kwa Yesu*

1 Yesu, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, anachoka ku mtsinje wa
Yorodani ndipo anatsogozedwa ndi Mzimu Woyerayo kupita ku chipululu,
2 kumene anayesedwa ndi mdierekezi masiku makumi anayi. Sanadye
kena kalikonse pa masiku amenewo, ndipo pa mapeto pake anamva njala.
3 Mdierekezi anati kwa Iye, "Ngati ndiwe Mwana wa Mulungu, uza
mwala uwu kuti usanduke buledi."
4 Yesu anayankha kuti, "Zalembedwa: 'Munthu sadzakhala ndi moyo
ndi chakudya chokha.' "
5 Mdierekezi anamutengera Iye pamalo aatali ndipo m'kamphindi
namuonetsa maufumu onse a dziko lapansi. 6 Ndipo anati kwa Iye,
"Ndidzakupatsani ulamuliro ndi ulemerero wawo; pakuti anandipatsa
ine, ndipo ndingathe kupereka kwa aliyense amene ndikufuna. 7 Ngati
mutandilambira, zonsezi zidzakhala zanu."
8 Yesu anayankha kuti, "Zalembedwa: 'Pembedza Yehova Mulungu wako
ndi kumutumikira Iye yekha.' "
9 Mdierekezi anapita naye ku Yerusalemu namuyimiritsa pamwamba
penipeni pa Nyumba ya Mulungu. Ndipo anati, "Ngati ndinu Mwana
wa Mulungu dziponyeni nokha pansi kuchokera pano. 10 Pakuti kwalem-
bedwa,
"Adzalamulira angelo ake za iwe
kuti akutchinjirize mosamala;
11 ndipo adzakunyamula ndi manja awo,
kuti phazi lako lisagunde pa mwala."
12 Yesu anayankha kuti, "Mawu akuti, 'Musamuyese Yehova Mulungu
wanu.' "
13 Mdierekezi atamaliza mayesero awa onse, anamusiya Iye kufikira
atapeza mpata wina.

*Yesu Akanidwa ku Nazareti*

14 Yesu anabwerera ku Galileya mu mphamvu ya Mzimu Woyera, ndipo
mbiri yake inafalikira ku madera onse a ku midzi. 15 Iye ankaphunzitsa
m'masunagoge awo, ndipo aliyense ankamulemekeza.
16 Iye anapita ku Nazareti, kumene anakulira, ndipo pa tsiku la
Sabata anakalowa m'sunagoge, monga mwa chikhalidwe chake. Ndipo
anayimirira kuti awerenge malemba. 17 Anamupatsa buku la mneneri
Yesaya. Atalitsekula, anapeza pamalo pamene panalembedwa kuti,
18 "Mzimu wa Ambuye ali pa Ine;
chifukwa wandidzoza
kuti ndilalikire Uthenga Wabwino kwa osauka.
Wandituma kuti ndilalikire kwa a m'ndende kuti amasulidwe

ndi kwa osaona kuti apenyenso,
kumasulidwa kwa osautsidwa,
19 ndi kulalikira za nthawi imene Ambuye adzakomere mtima anthu awo."

20 Kenaka Iye anatseka bukulo, nalibwezera kwa wotumikira ndipo
anakakhala pansi. Maso a aliyense m'sunagogemo anali pa Iye, 21 ndipo
anawawuza kuti, "Lero malemba awa akwaniritsidwa mmene mwamveramu."

22 Onse anayankhula zabwino za Iye ndipo anadabwa ndi mawu ogwira moyo amene anatuluka m'kamwa mwake. Iwo anafunsa kuti, "Kodi uyu si mwana wa Yosefe?"

23 Yesu anawawuza kuti, "Zoonadi, mudzandiwuza mwambi uwu: Sing'anga, dzichiritse wekha! Chitanso m'mudzi wa kwanu kuno zimene ife tamva kuti Iwe unazichita ku Kaperenawo."

24 Iye anapitiriza kuti, "Zoonadi, ndikukuwuzani kuti palibe mneneri
amene amavomerezedwa ku mudzi kwawo. 25 Ine ndikukutsimikizirani
kunali amayi ambiri amasiye mu Israeli m'nthawi ya Eliya, kumwamba
kutatsekedwa kwa zaka zitatu ndi theka ndipo kunali njala yayikulu
m'dziko lonselo. 26 Komabe Eliya sanatumidwe kwa mmodzi mwa iwo,
koma kwa mkazi wamasiye wa ku Zerefati ku chigawo cha Sidoni. 27 Ndipo
kunali akhate ambiri ku Israeli m'nthawi ya mneneri Elisa, koma panalibe
mmodzi mwa iwo anachiritsidwa kupatula Naamani wa ku Siriya."

28 Anthu onse m'sunagogemo anapsa mtima atamva izi. 29 Anayimirira
namutulutsira kunja kwa mzindawo, ndipo anamutengera pamwamba
pa phiri pamene mzindawo unamangidwapo, ndi cholinga chakuti
amuponyere ku phompho. 30 Koma Iye anangoyenda pakati pa gulu la
anthulo nachokapo.

### *Yesu Atulutsa Mzimu Woyipa*

31 Kenaka Iye anapita ku Kaperenawo, mudzi wa ku Galileya, ndipo pa
Sabata anayamba kuphunzitsa anthu. 32 Iwo anadabwa ndi chiphunzitso
chake chifukwa uthenga wake unali ndi ulamuliro.

33 M'sunagogemo munali munthu wogwidwa ndi mzimu woyipa. Iye
analira ndi mawu akulu, akuti 34 "Aa! Kodi mukufuna chiyani kwa ife,
Yesu wa ku Nazareti? Kodi mwabwera kudzatiwononga? Ndikudziwa kuti ndinu ndani, ndinu Woyerayo wa Mulungu!"

35 Yesu anachidzudzula kwambiri nati, "Khala chete! Tuluka mwa iye." Chiwandacho chinamugwetsa munthuyo pansi pamaso pa onse ndipo chinatuluka wosamupweteka.

36 Anthu onse anadabwa ndipo anati kwa wina ndi mnzake, "Kodi chiphunzitso ichi ndi chotani? Ndi ulamuliro ndi mphamvu Iye akulamulira
mizimu yoyipa ndipo ikutuluka!" 37 Ndipo mbiri yake inafalikira madera
onse ozungulira.

### *Yesu Achiritsa Anthu Ambiri*

38 Yesu anatuluka m'sunagoge ndipo anapita kwa Simoni. Tsopano mpongozi wake wa Simoni amadwala malungo akulu, ndipo anamupempha Yesu kuti amuthandize. 39 Ndipo anawerama nadzudzula malungowo
ndipo anamusiya. Anadzuka nthawi yomweyo nayamba kuwatumikira.

40 Pamene dzuwa linkalowa, anthu anabweretsa kwa Yesu onse amene
anali ndi matenda osiyanasiyana, ndipo atasanjika manja ake pa aliyense,

anachiritsidwa. [41] Komanso ziwanda zinkatuluka mwa anthu ambiri, zikufuwula kuti, "Inu ndinu Mwana wa Mulungu!" Koma Iye anazidzudzula ndipo sanazilole kuyankhula chifukwa zimadziwa kuti Iye ndi Khristu.

[42] Kutacha, Yesu anapita ku malo a yekha. Anthu ankamufunafuna
Iye ndipo pamene anafika kumene anali, anthuwo anayesetsa kumuletsa
kuti asawachokere. [43] Koma Iye anati, "Ine ndikuyenera kulalikira
Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu ku mizinda inanso chifukwa
ichi ndi chimene ananditumira." [44] Ndipo Iye anapitirirabe kulalikira
m'masunagoge a ku Yudeya.

# 5

*Yesu Ayitana Ophunzira Oyamba*

[1] Tsiku lina Yesu anayima m'mbali mwa nyanja ya Genesareti, gulu
la anthu litamuzungulira likumvetsera mawu a Mulungu. [2] Iye anaona
mabwato awiri ali m'mphepete mwa nyanja, asodzi amene ankachapa
makhoka awo atawasiya pamenepo. [3] Iye analowa m'bwato limodzi
limene linali la Simoni, ndi kumupempha kuti alikankhire m'kati mwa nyanja pang'ono. Kenaka Iye anakhala pansi nayamba kuphunzitsa anthu ali m'bwatomo.

[4] Atatha kuyankhula anati kwa Simoni, "Kankhirani kwa kuya ndipo muponye makhoka kuti mugwire nsomba."

[5] Simoni anayankha kuti, "Ambuye, tagwira ntchito molimbika usiku wonse, koma sitinagwire kanthu. Koma pakuti mwatero, ndiponya makhoka."

[6] Atachita izi, anagwira nsomba zambiri kotero kuti makhoka awo
anayamba kung'ambika. [7] Choncho anakodola anzawo a bwato linalo kuti abwere ndi kuwathandiza, ndipo anabwera nadzaza mabwato onse awiri mpaka kuyamba kumira.

[8] Simoni Petro ataona izi, anagwa pa mawondo a Yesu nati, "Chokani
kwa ine Ambuye: Ine ndine munthu wochimwa!" [9] Iye ndi anzake onse
anadabwa ndi nsomba zimene anagwira, [10] chimodzimodzinso Yakobo ndi Yohane, ana a Zebedayo, anzake a Simoniyo.

Kenaka Yesu anati kwa Simoni, "Musachite mantha; kuyambira tsopano
ndidzakusandutsani asodzi a anthu." [11] Kenaka anakokera mabwato awo ku mtunda, nasiya zonse namutsata Iye.

*Yesu Achiritsa Munthu Wakhate*

[12] Yesu ali ku mudzi wina, munthu amene anali ndi khate thupi lonse anabwera kwa Iye. Munthuyo ataona Yesu, anagwa chafufumimba ndipo anamupempha Iye kuti, "Ambuye, ngati mukufuna, mukhoza kundiyeretsa."

[13] Yesu anatambasula dzanja lake namukhudza munthuyo. Iye anati, "Ine ndikufuna, yeretsedwa!" Ndipo nthawi yomweyo khate lake linachoka.

[14] Kenaka Yesu anamulamula kuti, "Usawuze wina aliyense, koma pita, kadzionetse kwa wansembe ndi kukapereka nsembe zimene Mose anakulamulirani za kuyeretsedwa kwanu monga umboni kwa iwo."

[15] Koma mbiri yake inafalikirabe kwambiri kotero kuti magulu a anthu
anabwera kudzamvetsera ndi kuti achiritsidwe ku matenda awo. [16] Koma
Yesu nthawi zambiri ankachoka kupita ku malo a yekha kukapemphera.

*Yesu Achiritsa Wofa Ziwalo*

17 Tsiku lina pamene ankaphunzitsa, Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo,
amene anachokera ku midzi yonse ya Galileya ndi ku Yudeya ndi
Yerusalemu, anakhala pansi pomwepo. Ndipo mphamvu ya Ambuye
inalipo yakuti Iye achiritse odwala. 18 Amuna ena anabwera atanyamula
munthu wofa ziwalo pa mphasa ndipo anayesa kumulowetsa m'nyumba
kuti amugoneke pamaso pa Yesu. 19 Atalephera kupeza njira yochitira
zimenezi chifukwa cha gulu la anthu, anakwera naye pa denga ali
pa mphasa pomwepo ndi kumutsitsira m'kati pakati pa gulu la anthu,
patsogolo penipeni pa Yesu.

20 Yesu ataona chikhulupiriro chawo, anati, "Mnzanga, machimo ako
akhululukidwa."

21 Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo anayamba kuganiza mwa iwo okha
kuti, "Kodi munthu uyu ndi ndani amene ayankhula zamwano? Kodi
ndani amene angakhululukire machimo kupatula Mulungu?"

22 Yesu anadziwa zomwe iwo amaganiza ndipo anafunsa kuti, "Kodi
ndi chifukwa chiyani mukuganiza zimenezi m'mitima mwanu? 23 Kodi
chapafupi ndi chiti: kunena kuti, 'Machimo ako akhululukidwa,' kapena
kunena kuti, 'Nyamuka ndipo yenda?' " 24 Koma kuti inu mudziwe kuti
Mwana wa Munthu ali ndi ulamuliro pa dziko lapansi wokhululukira
machimo, Iye anati kwa munthu wofa ziwaloyo, "Ine ndikuwuza iwe kuti,
'Imirira, nyamula mphasa ndipo uzipita kwanu.' " 25 Nthawi yomweyo
anayimirira patsogolo pawo, nanyamula mphasa yake ndipo anapita
kwawo akuyamika Mulungu. 26 Aliyense anadabwa ndi kuchita mantha
ndipo anayamika Mulungu. Iwo anadabwa kwambiri ndipo anati, "Lero
taona zinthu zosayiwalika."

### *Kuyitanidwa kwa Levi*

27 Zitatha izi, Yesu anachoka ndipo anaona wolandira msonkho dzina
lake Levi atakhala m'nyumba ya msonkho. Yesu anati kwa iye, "Nditsate
Ine." 28 Ndipo Levi anayimirira, nasiya zonse ndi kumutsata Iye.

29 Kenaka Levi anakonzera Yesu phwando lalikulu ku nyumba yake
ndipo gulu lalikulu la amisonkho ndi ena ankadya naye pamodzi. 30 Koma
Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo amene anali a gulu lawo anadandaula
kwa ophunzira ake, "Kodi ndi chifukwa chiyani mukudya ndi kumwa
pamodzi ndi amisonkho ndi ochimwa?"

31 Yesu anawayankha kuti, "Amene sakudwala safuna sing'anga, koma
odwala. 32 Ine sindinabwere kudzayitana olungama, koma ochimwa kuti
atembenuke mtima."

### *Yesu Afunsidwa za Kusala Kudya*

33 Iwo anati kwa Iye, "Ophunzira a Yohane amasala kudya ndi kupem-
phera kawirikawiri, monganso ophunzira a Afarisi, koma anu amangodya
ndi kumwa."

34 Yesu anawayankha kuti, "Kodi alendo a mkwati angasale kudya
pamene mkwati ali pakati pawo? 35 Koma nthawi ikubwera pamene
mkwati adzachotsedwa pakati pawo. Masiku amenewo adzasala kudya."

36 Iye anawawuza fanizo ili: "Palibe amene amang'amba chigamba
kuchokera pa chovala chatsopano ndi kuchisokerera pa chakale. Ngati
atatero, ndiye kuti adzang'amba chovala chatsopanocho, ndipo chigamba
chochokera pa chovala chatsopano chija sichidzagwirizana ndi chakale.
37 Ndipo palibe amene amakhuthulira vinyo watsopano m'matumba a
vinyo akale. Ngati atatero, vinyo watsopanoyo adzaphulitsa zikopazo,

vinyo adzatayika ndipo zikopa za vinyozo zidzawonongeka. 38 Ayi, vinyo
watsopano ayenera kuthiridwa m'matumba a vinyo azikopa zatsopano.
39 Ndipo palibe amene atamwa vinyo wakale amafuna watsopano, pakuti
amati, 'Wakale ndi okoma.' "

# 6

*Yesu Mbuye wa Sabata*

1 Tsiku lina la Sabata Yesu ankadutsa m'minda yatirigu, ndipo ophunzira
ake anayamba kubudula ngala zatirigu, namazifikisa m'manja mwawo
ndi kumadya. 2 Ena mwa Afarisi anafunsa kuti, "Kodi n'chifukwa chiyani
mukuchita zosaloledwa pa tsiku la Sabata?"

3 Yesu anawayankha iwo kuti, "Kodi simunawerenge zimene Davide
anachita pamene iye ndi anzake anali ndi njala? 4 Iye analowa m'nyumba
ya Mulungu ndipo atatenga buledi wopatulika anadya amene ndi ololedwa
kudya ansembe okha. Ndipo anaperekanso wina kwa anzake." 5 Kenaka
Yesu anawawuza kuti, "Mwana wa Munthu ndi Ambuye wa Sabata."

6 La Sabata lina Iye analowa m'sunagoge kukaphunzitsa ndipo
m'menemo anapeza munthu wadzanja lolumala. 7 Afarisi ndi aphunzitsi
amalamulo ankamuyang'ana kuti apeze chifukwa Yesu, choncho ana-
muyang'anitsitsa kuti aone ngati Iye akanamuchiritsa pa Sabata. 8 Koma
Yesu anadziwa zimene ankaganiza ndipo anati kwa munthu wadzanja
lolumalayo, "Tanyamuka ndipo uyime patsogolo pa onsewa." Choncho
iye ananyamuka nayima pamenepo.

9 Kenaka Yesu anawawuza kuti, "Ndikufunseni, kodi chololedwa pa
Sabata ndi chiti: kuchita chabwino kapena kuchita choyipa, kupulumutsa
moyo kapena kuwononga?"

10 Iye atawayang'ana onsewo, anati kwa munthuyo, "Wongola dzanja
lako." Iye anaterodi, ndipo dzanja lake linachiritsidwa. 11 Koma
iwo anapsa mtima nayamba kukambirana wina ndi mnzake chomwe
akanamuchitira Yesu.

*Atumwi Khumi ndi Awiri*

12 Tsiku lina, masiku amenewo, Yesu anapita ku phiri kukapemphera
ndipo anakhala usiku wonse akupemphera kwa Mulungu. 13 Kutacha,
anayitana ophunzira ake ndipo anasankha khumi ndi awiri a iwo amene
anawayika kukhala atumwi: 14 Simoni (amene anamutcha Petro), m'bale
wake wa Andreya, Yakobo, Yohane, Filipo, Bartumeyu, 15 Mateyu, Tomasi,
Yakobo mwana wa Alufeyo, Simoni amene amatchedwa Zaleti, 16 Yudasi
mwana wa Yakobo ndi Yudasi Isikarioti amene anamupereka.

*Madalitso ndi Tsoka*

17 Iye anatsika pamodzi ndi atumwiwo ndipo anayima pamalo athyathy-
athya. Gulu lalikulu la ophunzira ake, gulu lalikulu la anthu ochokera
ku Yudeya konse, ku Yerusalemu ndi ochokera m'mphepete mwa nyanja
ya Turo ndi Sidoni anali pomwepo. 18 Iwo anabwera kudzamvetsera
ndi kuchiritsidwa ku matenda awo. Osautsidwa ndi mizimu yoyipa
anachiritsidwa, 19 ndipo anthu ankayesetsa kuti amukhudze chifukwa
mphamvu imatuluka mwa Iye ndi kuchiritsa onse.

20 Akuyang'ana ophunzira ake, Iye anati,

"Odala ndinu amene ndi osauka,
chifukwa ufumu wa Mulungu ndi wanu.
21 Inu amene mukumva njala tsopano, ndinu odala

chifukwa mudzakhutitsidwa.
Inu amene mukulira tsopano, ndinu odala
chifukwa mudzasekerera.
22 Ndinu odala, anthu akamakudani,
kukusalani ndi kukunyozani
ndi kumayipitsa dzina lanu chifukwa cha Mwana wa Munthu.
23 “Nthawi imeneyo sangalalani ndipo lumphani ndi chimwemwe chi-
fukwa mphotho yanu ndi yayikulu kumwamba. Pakuti ndi zomwezonso
zimene makolo awo anachitira aneneri.
24 “Ndinu atsoka, anthu olemera,
popeza mwalandiriratu zokusangalatsani.
25 Tsoka inu amene mukudya bwino tsopano,
chifukwa mudzakhala ndi njala.
Ndinu atsoka, amene mukusekerera tsopano,
chifukwa mudzabuma ndi kulira.
26 Ndinu atsoka, anthu akamakuyamikirani,
popeza makolo anu anawachitira aneneri onama zomwezi.”

### *Kukonda Adani*

27 “Koma Ine ndikuwuza inu amene mukundimvra: Kondani adani anu,
chitirani zabwino amene amakudani. 28 Dalitsani amene amakutember-
erani, apemphererani amene amakusautsani. 29 Ngati wina akumenyani
patsaya limodzi mupatseninso tsaya linalo. Ngati wina akulanda mwin-
jiro wako, umulole atenge ndi mkanjo omwe. 30 Mupatseni aliyense
amene akupemphani kanthu ndipo ngati wina atenga chinthu chanu,
musamulamule kuti akubwezereni. 31 Inu muwachitire anthu ena, zomwe
mukanafuna kuti iwo akuchitireni.
32 “Ngati mukonda okhawo amene amakukondani, mwapindula
chiyani? Ngakhale ‘ochimwa’ amakonda amene amawakondanso.
33 Ndipo ngati muchita zabwino kwa amene ndi abwino kwa inu,
mwapindula chiyani? Ngakhale ‘ochimwa’ amachita izi. 34 Ndipo
ngati mukongoza amene mukuyembekeza kuti abweza, mwapindula
chiyani? Ngakhale ‘ochimwa’ amabwereketsa kwa ochimwa anzawo,
ndipo amayembekezera kubwezeredwa zonse. 35 Koma kondani adani
anu, achitireni zabwino, akongozeni koma osayembekezera kulandira
kanthu. Pamenepo mphotho yanu idzakhala yayikulu ndipo inu mudza-
khala ana a Wammwambamwamba, chifukwa ndi wokoma mtima kwa
anthu osayamika ndi oyipa. 36 Khalani achifundo, monga momwe Atate
anu ali achifundo.”

### *Za Kuweruza Ena*

37 “Musaweruze, ndipo inu simudzaweruzidwa. Musatsutse ndipo
inu simudzatsutsidwa. Khululukirani ena ndipo mudzakhululukidwa.
38 Perekani ndipo mudzapatsidwa. Adzakupatsani m’thumba mwanu
muyeso wabwino, wotsenderezeka, wokhutchumuka ndi wosefukira.
Pakuti muyeso umene mumagwiritsa ntchito, ndi omwewo adzakuye-
serani.”
39 Iye anawawuzanso fanizo ili, “Kodi munthu wakhungu angatso-
golere munthu wakhungu mnzake? Kodi onse sadzagwera m’dzenje?
40 Wophunzira sangapose mphunzitsi wake, koma yense amene waphun-
zitsidwa bwinobwino adzakhala ngati mphunzitsi wake.
41 “Kodi ndi chifukwa chiyani mumaona kachitsotso m’diso la m’bale
wanu ndi kusasamala mtengo uli m’diso mwanu? 42 Kodi munganene

bwanji kwa m'bale wanu kuti, 'M'bale n'takuchotsa kachitsotso m'diso mwako,' pamene inu eni ake mukulephera kuona mtengo uli m'diso mwanu? Inu achiphamaso, yambani mwachotsa mtengo uli m'diso mwanu, ndipo kenaka mudzaona bwinobwino ndi kuchotsa kachitsotso m'diso la m'bale wanu."

### *Mtengo ndi Zipatso Zake*

43 Palibe mtengo wabwino umene umabala chipatso choyipa, kapena
mtengo oyipa umene umabala chipatso chabwino. 44 Mtengo uliwonse
umadziwika ndi chipatso chake. Anthu sathyola nkhuyu pa mtengo
waminga, kapena mphesa pa nthungwi. 45 Munthu wabwino amatulutsa
zinthu zabwino zosungidwa mu mtima mwake, koma munthu oyipa amatulutsa zinthu zoyipa zosungidwa mu mtima mwake. Pakamwa pake pamayankhula zimene zadzaza mu mtima mwake.

### *Womanga Nyumba Wanzeru ndi Wopusa*

46 "Kodi n'chifukwa chiyani munditchula kuti, 'Ambuye, Ambuye' koma
simuchita zimene Ine ndinena? 47 Ine ndidzakuonetsani mmene alili
munthu amene amabwera kwa Ine ndi kumva mawu anga ndi kuwachita.
48 Iye ali ngati munthu womanga nyumba, amene anakumba mozama
nayika maziko ake pa mwala. Madzi osefukira atabwera ndi mphamvu,
nawomba nyumbayo koma sinagwedezeka, chifukwa anayimanga bwino.
49 Koma amene amamva mawu anga koma osawachita, akufanana ndi
munthu amene anamanga nyumba yake koma yopanda maziko. Nthawi yomwe madziwo anawomba nyumbayo, inagwa ndipo inawonongekeratu."

## 7

### *Chikhulupiriro cha Kenturiyo*

1 Yesu atamaliza kunena zonsezi pamaso pa anthu amene ankamvetsera,
analowa mu Kaperenawo. 2 Kumeneko wantchito wa Kenturiyo,
amene amamukhulupirira kwambiri, anadwala ndipo anali pafupi kufa.
3 Kenturiyo anamva za Yesu ndipo anatumiza ena a akulu Ayuda kwa
Iye kuti abwere adzachiritse wantchito wakeyo. 4 Iwo atafika kwa Yesu,
anamudandaulira kwambiri, nati, "Munthuyu ayenera kuthandizidwa
5 chifukwa amakonda mtundu wathu ndipo anatimangira sunagoge
wathu." 6 Pamenepo Yesu anapita nawo.
Iye sanali patali ndi nyumba pamene Kenturiyo anatumiza anzake kuti akamuwuze kuti, "Ambuye, musadzivutitse, pakuti ndine wosayenera kuti
mulowe m'nyumba mwanga. 7 N'chifukwa chake sindinadziyenereze ndi
pang'ono pomwe kuti ndibwere kwa inu. Koma nenani mawu, ndipo
wantchito wanga adzachira. 8 Pakuti ndili pansi paulamuliro, ndiponso
ndili ndi asilikali pansi panga. Ndikamuwuza uyu kuti, 'Pita,' iye amapita; ndi uyo kuti, 'Bwera,' amabwera. Ndikamuwuza wantchito wanga kuti, 'Chita ichi,' amachita."
9 Yesu atamva izi, anadabwa naye, ndipo anatembenukira gulu la
anthu limene limamutsatira nati, "Ndikukuwuzani kuti, sindinapeze
chikhulupiriro chachikulu ngati ichi mu Israeli." 10 Kenaka anthu amene
anatumidwawo anabwerera ku nyumba ndipo anakamupeza wantchitoyo atachira.

### *Yesu Aukitsa Mwana wa Mayi Wamasiye*

11 Zitangotha izi, Yesu anapita ku mudzi wa Naini ndipo ophunzira ake
ndi gulu lalikulu la anthu linapita naye pamodzi. 12 Akufika pa chipata cha
mudziwo, anakumana ndi anthu amene ankatuluka ndi munthu wakufa
amene anali mwana yekhayo wa mkazi wamasiye. Gulu lalikulu la anthu
a m'mudziwo linali naye. 13 Ambuye atamuona mayiyo, mtima wawo
unagwidwa naye chifundo ndipo anati, "Usalire."
14 Kenaka anapita nakakhudza chithatha cha maliro ndipo amene
anachinyamulawo anayima. Iye anati, "Mnyamata, ndikukuwuza kuti,
dzuka!" 15 Wakufayo anakhala tsonga ndi kuyamba kuyankhula, ndipo
Yesu anamupereka mnyamatayo kwa amayi ake.
16 Onse anachita mantha kwambiri nalemekeza Mulungu. Iwo anati,
"Mneneri wamkulu waonekera pakati pathu. Mulungu wabwera kudza-
thandiza anthu ake." 17 Mbiriyi inafalikira ku Yudeya konse ndi ku madera
ozungulira.

### *Yesu ndi Yohane M'batizi*

18 Ndipo ophunzira a Yohane anamuwuza Yohaneyo zinthu zonsezi.
Atayitana awiri a ophunzirawo, 19 anawatumiza kwa Ambuye kukafunsa
kuti, "Kodi ndinu anayenera kubwerayo, kapena tiyembekezere wina?"
20 Anthuwo atafika kwa Yesu anati, "Yohane M'batizi watituma kwa
Inu kuti tidzafunse kuti, 'Kodi ndinu anayenera kubwerayo, kapena
tiyembekezere wina?' "
21 Pa nthawi yomweyo, Yesu anachiritsa ambiri amene ankavutika,
odwala ndi amene anali mizimu yoyipa, ndiponso anapenyetsa anthu
osaona. 22 Ndipo Iye anawayankha otumidwawo kuti, "Bwererani ndi
kukamuwuza Yohane zimene mwaona ndi kumva: Osaona akuona,
olumala akuyenda, akhate akuchiritsidwa, osamva akumva, akufa akuuk-
itsidwa, ndipo Uthenga Wabwino ukulalikidwa kwa osauka. 23 Odala
munthu amene sakhumudwa chifukwa cha Ine."
24 Anthu otumidwa ndi Yohane aja atachoka, Yesu anayamba
kuyankhula ndi gulu la anthu za Yohaneyo kuti, "Kodi munkapita ku
chipululu kukaona chiyani? Bango logwedezeka ndi mphepo? 25 Ngati si
choncho, munkapita kukaona chiyani? Munthu wovala zovala zabwino?
Ayi, ovala zovala zodula ndi okhala moyo wapamwamba ali m'nyumba
zaufumu. 26 Koma inu munkapita kukaona chiyani? Mneneri? Inde, Ine
ndikukuwuzani, woposa mneneri. 27 Uyu ndi amene malemba akunena
za Iye kuti,
" 'Ine ndidzatuma mthenga wanga patsogolo panu,
amene adzakonza njira yanu.'
28 Ine ndikukuwuzani kuti pakati pa obadwa kuchokera mwa mkazi palibe
wina wamkulu kuposa Yohane; komabe amene ali wamng'ono mu ufumu
wa Mulungu ndi wamkulu kuposa iye."
29 Anthu onse, ngakhale amisonkho, atamva mawu a Yesu, anavomereza
kuti njira ya Mulungu ndi yolondola, chifukwa anabatizidwa ndi Yohane.
30 Koma Afarisi ndi akatswiri amalamulo anakana cholinga cha Mulungu
kwa iwo okha, chifukwa sanabatizidwe ndi Yohane.
31 "Kodi ndingawafanizire chiyani anthu a m'bado uno? Ali ngati
chiyani? 32 Ali ngati ana amene akukangana pa msika, ena akufunsa
anzawo kuti,
" 'Ife tinakuyimbirani chitoliro,
koma inu simunavine.
Tinakuyimbirani nyimbo zamaliro,

koma inu simunalire.'
33 Pakuti Yohane M'batizi sanabwere kudzadya buledi kapena kumwa
vinyo, koma inu mumati, 'Ali ndi chiwanda.' 34 Mwana wa Munthu
anabwera nadya ndi kumwa, ndipo inu mukuti, 'Ali ndi dyera komanso
ndi woledzera, bwenzi la amisonkho ndi ochimwa.' 35 Ndipo nzeru
zimaoneka zolondola mwa ana ake onse."

*Yesu Adzozedwa ndi Mayi Wochimwa*

36 Tsopano mmodzi mwa Afarisi anayitana Yesu kuti akadye naye ku
nyumba kwake ndipo anapita nakakhala pa tebulo. 37 Mayi amene
amakhala moyo wauchimo mu mzindawo atadziwa kuti Yesu akudya ku
nyumba ya Mfarisiyo, anabweretsa botolo la mafuta onunkhira a alabasta.
38 Iye anayimirira kumbuyo kwa Yesu pa mapazi ake akulira, nayamba
kumadontheza misozi pa mapazi ake. Ndipo iye anapukuta mapaziwo
ndi tsitsi lake, nawapsompsona ndi kuwathira mafuta onunkhirawo.

39 Mfarisiyo anamuyitanayo ataona izi, anati mu mtima mwake, "Ngati munthuyu akanakhala mneneri, akanadziwa kuti akumukhudzayo ndi mayi otani, kuti ndi wochimwa."

40 Yesu anamuyankha iye kuti, "Simoni, ndili ndi kanthu koti ndikuwuze."

Iye anati, "Ndiwuzeni Aphunzitsi."

41 "Anthu awiri anakongola ndalama kwa munthu wina wokongoletsa
ndalama: mmodzi ndalama zokwana 500 ndi winayo ndalama makumi
asanu. 42 Panalibe mmodzi mwa iwo anali ndi ndalama zobwezera, ndipo
iye anawakhululukira ngongole zawo. Tsopano ndi ndani mwa awiriwa
adzamukonde koposa?"

43 Simoni anayankha kuti, "Ndikuganiza kuti ndi amene anamukhululukira ngongole yayikulu."

Yesu anati, "Wayankha molondola."

44 Kenaka anatembenukira kwa mayiyo nati kwa Simoni, "Ukumuona
mayiyu? Ine ndabwera m'nyumba yako. Iwe sunandipatse madzi otsukira
mapazi anga, koma iyeyu wanyowetsa mapazi anga ndi misozi yake ndi
kuwapukuta ndi tsitsi lake. 45 Iwe sunandipsompsone, koma mayiyu,
kuyambira pamene Ine ndalowa, sanaleke kupsompsona mapazi anga.
46 Iwe sunadzoze mutu wanga mafuta, koma iye wadzoza mapazi anga
mafuta onunkhira. 47 Tsono, ndikukuwuza iwe, machimo ake amene ndi
ambiri akhululukidwa, monga chaonetsera chikondi chake chachikulu.
Koma iye amene wakhululukidwa zochepa amakonda pang'ono."

48 Kenaka anati kwa mayiyo, "Machimo ako akhululukidwa."

49 Alendo enawo anayamba kumanena m'mitima mwawo kuti, "Uyu ndi ndani amene akhululukiranso machimo?"

50 Yesu anati kwa mayiyo, "Chikhulupiriro chako chakupulumutsa. Pita mu mtendere."

# 8

*Fanizo la Wofesa*

1 Zitatha izi, Yesu anayendayenda kuchoka mzinda wina kupita wina
ndiponso mudzi wina kupita wina, akulalikira Uthenga Wabwino wa
ufumu wa Mulungu. Ophunzira ake khumi ndi awiri aja anali naye,
2 komanso akazi ena amene anachiritsidwa ku mizimu yoyipa ndi
matenda: Mariya, wotchedwa Magadalena, amene mwa iye munatuluka
ziwanda zisanu ndi ziwiri; 3 Yohana mkazi wa Kuza, woyang'anira

m'nyumba ya Herode; Suzana; ndi ena ambiri analinso. Akazi awa ankawathandiza ndi chuma chawo.
4 Anthu ambiri ankasonkhana, ndipo pamene anthu ankabwera kwa Yesu kuchokera ku midzi, Iye anawawuza fanizo ili, 5 "Mlimi anapita
kukafesa mbewu zake. Akufesa mbewuzo, zina zinagwa m'mbali mwa njira; zinapondedwa, ndipo mbalame zamlengalenga zinadya. 6 Zina zi-
nagwa pa thanthwe, ndipo pamene zinamera, zinafota chifukwa panalibe chinyezi. 7 Mbewu zina zinagwera pakati pa minga, zinakulira pamodzi
ndi mingazo ndipo zinalepheretsa mmerawo kukula. 8 Mbewu zina
zinagwera pa nthaka yabwino. Zinamera ndipo zinabala mowirikiza 100 kuposa zimene zinafesedwa zija."
Atanena izi, anafuwula kuti, "Amene ali ndi makutu, amve."
9 Ophunzira ake anamufunsa tanthauzo lake la fanizolo. 10 Iye anati,
"Kudziwa zinsinsi za ufumu wa Mulungu kwapatsidwa kwa inu, koma kwa ena ndimawayankhula m'mafanizo kuti,

"ngakhale akuona, asapenye;
ngakhale akumva, asazindikire."

11 "Tanthauzo la fanizoli ndi ili: Mbewu ndi mawu a Mulungu. 12 Mbewu
za m'mbali mwa njira ndi anthu amene amamva mawu, ndipo kenaka mdierekezi amabwera ndi kuchotsa mawuwo m'mitima mwawo kuti asakhulupirire ndi kupulumutsidwa. 13 Mbewu za pa thanthwe ndi
anthu amene amalandira mawu mwachimwemwe pamene akumva, koma mawuwo sazika mizu. Iwo amakhulupirira kwa kanthawi, koma pa nthawi ya mayesero, amagwa. 14 Mbewu zimene zinagwa pakati pa minga
zikuyimira anthu amene amamva mawu, koma akamayenda m'njira zawo amatsamwitsidwa ndi zodandaulitsa za moyo uno, chuma ndi zosangalatsa, ndipo iwo samakhwima. 15 Koma mbewu za pa nthaka
yabwino zikuyimira anthu amene ali ndi mtima woona ndi wabwino, amene amamva mawu nawasunga, ndipo amalimbikira mpaka amabala zipatso.

### *Nyale ndi Choyikapo Chake*

16 "Palibe amayatsa nyale ndi kuyibisa mu mtsuko kapena kuyika
pansi pa bedi. Koma m'malo mwake, amayika pa choyikapo chake, kuti anthu olowamo aone kuwala. 17 Pakuti palibe kanthu kobisika kamene
sikadzawululika, ndipo palibe kanthu kophimbika kamene sikadzadzi-wika kapena kuonetsedwa poyera. 18 Choncho ganizirani mozama. Iye
amene ali nazo adzapatsidwa zambiri, iye amene alibe, ngakhale chimene akuganiza kuti ali nacho adzalandidwa."

### *Amayi ndi Abale a Yesu*

19 Tsopano amayi ndi abale a Yesu anabwera kudzamuona Iye, koma
analephera kuti afike pafupi ndi Iye chifukwa cha gulu la anthu. 20 Wina
anamuwuza Iye kuti, "Amayi ndi abale anu ayima kunja, akufuna kukuonani."
21 Yesu anayankha kuti, "Amayi ndi abale anga ndi amene amamva mawu a Mulungu ndi kumachita zimene mawuwo akunena."

### *Yesu Aletsa Namondwe*

22 Tsiku lina Yesu anati kwa ophunzira ake, "Tiyeni tiwolokere tsidya
lina la nyanja." Ndipo analowa m'bwato nanyamuka. 23 Akuwoloka, Iye
anagona tulo. Namondwe wamkulu anayamba pa nyanja, ndipo bwatolo linayamba kudzaza ndi madzi ndipo anali pa chiopsezo chachikulu.

24 Ophunzira anapita ndi kukamudzutsa Iye, nati, “Ambuye, Ambuye,
ife tikumira!”
Anadzuka ndipo anadzudzula mphepo ndi madzi owindukawo. Na-
mondwe anasiya, ndipo panali bata. 25 Iye anafunsa ophunzira ake kuti,
“Chikhulupiriro chanu chili kuti?”
Koma pogwidwa ndi mantha ndi kudabwa anafunsana wina ndi mnzake
kuti, “Uyu ndi ndani? Iye alamulira ngakhale mphepo ndi madzi, ndipo
zimumvera Iye.”

### *Achiritsidwa Munthu Wogwidwa ndi Ziwanda*

26 Iwo anawolokera ku chigawo cha Gerasa chimene chili tsidya lina la
nyanja kuchokera ku Galileya. 27 Yesu ataponda pa mtunda, anakumana
ndi munthu wogwidwa ndi ziwanda wochokera mu mzindawo. Kwa
nthawi yayitali munthuyu sanavale zovala kapena kukhala m’nyumba,
koma amakhala ku manda. 28 Iye ataona Yesu, anakuwa nagwa pa
mapazi ake akufuwula kwambiri kuti, “Mukufuna chiyani ndi ine, Yesu
Mwana wa Mulungu Wammwambamwamba? Ndikupemphani Inu, mu-
sandizunze ine!” 29 Pakuti Yesu analamula mzimu woyipawo kuti utuluke
mwa munthuyo. Kawirikawiri umamugwira iye, ndipo ngakhale anali
womangidwa ndi unyolo dzanja ndi mwendo ndi kuti ankamuyang’anira,
koma amadula maunyolo akewo ndipo ziwanda zimamutengera kumalo
a yekha.
30 Yesu anamufunsa kuti, “Dzina lako ndani?”
Iye anayankha kuti, “Legiyo,” chifukwa ziwanda zambiri zinalowa
mwa iye. 31 Ndipo ziwandazo zimamupempha mobwerezabwereza kuti
asazitumize ku dzenje la mdima.
32 Gulu lalikulu la nkhumba limadya pamenepo m’mbali mwa phiri.
Ziwandazo zinamupempha Yesu kuti azilole kuti zikalowe mu nkhumbazo
ndipo Iye anazilola. 33 Ziwanda zija zitatuluka mwa munthuyo, zi-
nakalowa mwa nkhumbazo, ndipo gulu lonselo linathamangira ku mtsetse
ndi kukalowa m’nyanja ndi kumira.
34 Oweta nkhumbazo ataona zimene zinachitikazo, anathamanga ndi
kukanena izi mu mzinda ndi ku madera a ku midzi. 35 Ndipo anthu
anapita kukaona zimene zinachitika. Atafika kwa Yesu, anapeza munthu
amene anatulutsidwa ziwanda uja atakhala pa mapazi a Yesu, atavala
ndipo ali ndi nzeru zake; ndipo iwo anachita mantha. 36 Amene
anaona izi anawuza anthu mmene munthu wogwidwa ndi ziwandayo
anachiritsidwira. 37 Kenaka anthu onse a ku chigawo cha Gerasa
anamupempha Yesu kuti achoke kwa iwo, chifukwa anadzazidwa ndi
mantha. Choncho Iye analowa m’bwato nachoka.
38 Munthu amene anatulutsidwa ziwanda uja, anapempha Yesu kuti
apite nawo, koma Yesu anamubweza nati, 39 “Bwerera kwanu kafotokoze
zimene Mulungu wakuchitira.” Ndipo munthuyo anachoka ndi kukanena
ku mzinda wonsewo zimene Yesu anamuchitira iye.

### *Mwana Wamkazi wa Yairo ndi Mayi Wokhudza Chovala cha Yesu*

40 Yesu atabwerera, gulu lalikulu la anthu linamulandira, chifukwa onse
ankamuyembekezera. 41 Nthawi yomweyo munthu wotchedwa Yairo,
woweruza wa mu sunagoge, anabwera ndi kugwa pa mapazi a Yesu,
namupempha Iye kuti apite ku nyumba kwake, 42 chifukwa mwana wake
yekhayo wamkazi, kamtsikana ka zaka khumi ndi ziwiri, kanali pafupi
kufa.

Pamene Yesu ankapita gulu la anthu linkamupanikiza. 43 Ndipo
pomwepo panali mayi wina amene ankataya magazi kwa zaka khumi
ndi ziwiri, koma panalibe wina akanamuchiritsa. 44 Iye anafika kumbuyo
kwake ndi kukhudza mothera mwa chovala chake, ndipo nthawi yomweyo
magazi ake analeka kutuluka.

45 Yesu anafunsa kuti, "Wandikhudza ndani?"

Onse atakana, Petro anati, "Anthu akukupanikizani ndi kukukankhani."

46 Koma Yesu anati, "Wina wandikhudza; ndikudziwa chifukwa
mphamvu yachoka mwa Ine."

47 Ndipo mayiyo podziwa kuti sanathe kuchoka wosadziwika, anabwera
akunjenjemera ndipo anagwa pa mapazi a Yesu. Pamaso pa anthu
onse, anafotokoza chifukwa chimene anamukhudzira Iye ndi mmene iye
anachiritsidwira nthawi yomweyo. 48 Kenaka anati kwa iye, "Mwana
wamkazi, chikhulupiriro chako chakuchiritsa. Pita mu mtendere."

49 Pamene Yesu ankayankhulabe, munthu wina anabwera kuchokera ku
nyumba ya Yairo, woweruza wa ku sunagoge uja. Iye anati, "Mwana wanu
wa mkazi wamwalira, musawavutitsenso Aphunzitsiwa."

50 Atamva zimenezi, Yesu anati kwa Yairo, "Usachite mantha, ingokhulupirira basi ndipo adzachiritsidwa."

51 Iye atafika ku nyumba ya Yairo, sanalole wina aliyense kulowa
kupatula Petro, Yohane, ndi Yakobo ndi abambo ndi amayi a mwanayo.
52 Pa nthawiyi n'kuti anthu onse akubuma ndi kumulirira iye. Yesu anati,
"Lekani kulira, sanafe koma wagona tulo."

53 Iwo anamuseka podziwa kuti anali atamwalira. 54 Koma Iye
anamugwira dzanja lake ndipo anati, "Mwana wanga, dzuka!" 55 Mzimu
wake unabwerera, ndipo nthawi yomweyo anayimirira. Kenaka Yesu
anawawuza kuti amupatse chakudya. 56 Makolo ake anadabwa, koma Iye
anawalamulira kuti asawuze wina aliyense zimene zinachitikazo.

# 9

*Yesu Atuma Ophunzira ake Khumi ndi Awiri*

1 Yesu atawayitana khumi ndi awiriwo pamodzi, Iye anawapatsa
mphamvu ndi ulamuliro wotulutsa ziwanda zonse ndi kuchiritsa matenda.
2 Ndipo Iye anawatumiza kukalalikira za ufumu wa Mulungu
ndi kukachiritsa odwala. 3 Iye anawawuza kuti, "Musatenge kanthu
paulendo. Musatenge ndodo, thumba, buledi, ndalama, ndi malaya
apadera. 4 Nyumba iliyonse imene mulowa, mukhale momwemo kufikira
mutachoka mu mzindawo. 5 Ngati anthu sakulandirani, sasani fumbi
la kumapazi anu pomwe mukuchoka mu mzinda wawo ngati umboni
owatsutsa." 6 Ndipo iwo ananyamuka napita, mudzi ndi mudzi, kulalikira
Uthenga Wabwino ndi kuchiritsa anthu paliponse.

7 Tsopano Herode olamulirayo anamva zonse zimachitikazi. Ndipo iye
anavutika kwambiri chifukwa ena amati Yohane waukitsidwa kwa akufa,
8 ena amati Eliya waonekera, ndipo ena anatinso mmodzi wa aneneri
akalekale waukanso. 9 Koma Herode anati, "Ine ndinamudula mutu
Yohane. Nanga uyu ndani amene ndikumva zinthu zotere za Iye?" Ndipo
iye anayesetsa kuti amuone Iye.

*Yesu Adyetsa Anthu 5,000*

10 Atumwi atabwerera, anamuwuza Yesu zimene anachita. Kenaka Iye
anawatenga napita kwa okha ku mudzi wa Betisaida. 11 Koma gulu la

anthu linadziwa ndipo anamutsatira. Iye anawalandira ndi kuyankhula
nawo za ufumu wa Mulungu, ndi kuchiritsa amene amafuna machiritso.
12 Chakumadzulo dzuwa litapita, khumi ndi awiriwo anabwera kwa
Iye ndipo anati, "Uzani gulu la anthuli lichoke kuti apite ku midzi
yotizungulira ndi madera a ku mudzi kuti akapeze chakudya ndi pogona,
chifukwa kuno ndi kuthengo."
13 Iye anayankha kuti, "Apatseni chakudya kuti adye."
Iwo anayankha kuti, "Ife tili ndi malofu a buledi asanu okha ndi nsomba
ziwiri, pokhapokha titapita kukagula chakudya cha gulu la anthu onsewa."
14 (Pamenepo panali amuna pafupifupi 5,000).
Koma Iye anati kwa ophunzira ake, "Akhazikeni pansi m'magulu a
anthu pafupifupi makumi asanu." 15 Ophunzira ake anachita zomwezo
ndipo aliyense anakhala pansi. 16 Atatenga malofu a buledi asanu ndi
nsomba ziwiri zija anayang'ana kumwamba, nayamika ndipo anazigawa.
Kenaka anazipereka kwa ophunzira ake kuti azipereke kwa anthu. 17 Onse
anadya nakhuta, ndipo ophunzira ake anatolera madengu khumi ndi awiri
odzaza ndi nyenyeswa zomwe zinatsala.

### *Petro Avomereza Khristu*

18 Nthawi ina pamene Yesu amapemphera malo a yekha ali ndi
ophunzira ake, Iye anawafunsa kuti, "Kodi anthu amati Ine ndine yani?"
19 Iwo anayankha kuti, "Ena amati Yohane M'batizi; ena amati Eliya;
ndipo enanso amati mmodzi wa aneneri akalekale waukanso."
20 Iye anafunsa kuti, "Koma nanga inu mumati Ine ndine yani?"
Petro anayankha kuti, "Mpulumutsi wolonjezedwa uja wa Mulungu."

### *Yesu Aneneratu za Imfa yake*

21 Yesu anawachenjeza kwambiri kuti asawuze wina aliyense za izi.
22 Ndipo Iye anati, "Mwana wa Munthu ayenera kuzunzika kwambiri ndi
kukanidwa ndi akulu a ansembe ndi aphunzitsi amalamulo, Iye ayenera
kuphedwa ndipo tsiku lachitatu adzauka kwa akufa."
23 Ndipo Iye anawuza onse kuti, "Ngati wina aliyense akufuna kutsata
Ine, ayenera kudzikana yekha ndi kusenza mtanda wake tsiku ndi tsiku
n'kumanditsata Ine. 24 Popeza aliyense amene akufuna kupulumutsa
moyo wake adzawutaya, koma aliyense amene adzataya moyo wake
chifukwa cha Ine adzawupulumutsa. 25 Kodi chabwino ndi chiti kwa
munthu, kupata zonse zapansi pano, koma ndi kutaya moyo wake kapena
kudziwononga iye mwini? 26 Ngati wina aliyense achita nane manyazi
ndi ndiponso mawu anga, Mwana wa Munthu adzachita naye manyazi
pamene adzabwera mu ulemerero wake ndi mu ulemerero wa Atate ndi
angelo oyera. 27 Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti ena mwa inu amene
mwayima pano simudzalawa imfa musanaone ufumu wa Mulungu."

### *Maonekedwe a Ulemerero wa Yesu pa Phiri*

28 Patatha pafupifupi masiku asanu ndi atatu Yesu atanena izi, Iye
anatenga Petro, Yohane ndi Yakobo ndi kukwera ku phiri kukapemphera.
29 Pamene Iye ankapemphera, maonekedwe a nkhope yake, ndi zovala
zake zinawala monyezimira kwambiri. 30 Anthu awiri, Mose ndi Eliya,
31 anaonekera mu ulemerero opambana akuyankhulana ndi Yesu. Iwo
amayankhulana za kuchoka kwake, kumene Iye anali pafupi kukakwanir-
itsa ku Yerusalemu. 32 Petro ndi anzake anali ndi tulo tambiri, koma
atadzuka, iwo anaona ulemerero wake ndi anthu awiri atayima pamodzi

ndi Iye. 33 Pamene anthuwo ankamusiya Yesu, Petro anati kwa Iye,
“Ambuye, ndi chabwino kwa ife kuti tikhale pano. Tiloleni kuti timange
misasa itatu, umodzi wanu, umodzi wa Mose ndi umodzi wa Eliya.” (Iye
sanadziwe chimene amayankhula).

34 Pamene Iye ankayankhula, mtambo unaonekera ndi kuwaphimba
iwo, ndipo anachita mantha pamene mtambowo unawakuta. 35 Mawu
anachokera mu mtambomo nati, “Uyu ndi Mwana wanga amene ndamu-
sankha; mumvereni Iye.” 36 Atamveka mawuwa, anaona kuti Yesu anali
yekha. Ophunzirawo anazisunga izi mwa iwo okha ndipo sanawuze wina
aliyense pa nthawiyi za zomwe iwo anaziona.

### *Kuchiritsidwa kwa Mwana Wogwidwa ndi Chiwanda*

37 Mmawa mwake, akutsika ku phiri, anthu ambiri anakumana naye.
38 Munthu wina m’gulu la anthulo anayitana kuti, “Aphunzitsi, ndiku-
pemphani kuti muone mwana wangayu, pakuti ndi mmodzi yekhayu.
39 Chiwanda chikamugwira amafuwula mwadzidzidzi; chimamugwedeza
kolimba mpaka kutuluka thovu kukamwa. Sichimusiya ndipo chikumu-
wononga. 40 Ine ndinapempha ophunzira anu kuti achitulutse, koma
alephera.”

41 Yesu anayankha kuti, “Haa! Anthu osakhulupirira ndi m’bado
wokhota. Kodi Ine ndidzakhala nanu nthawi yayitali yotani ndi kukupiri-
rani? Bweretsa mwana wako kuno.”

42 Ngakhale pamene mnyamata amabwera kwa Yesu, chiwandacho
chinamugwetsa pansi ndi kumugwedeza. Koma Yesu anadzudzula mzimu
woyipawo nachiritsa mwa mnyamatayo ndi kumuperekanso kwa abambo
ake. 43 Ndipo iwo onse anadabwa ndi ukulu wa Mulungu.

### *Yesu Abwereza Kunena za Imfa yake*

Aliyense akudabwa ndi zimene Yesu anachita, Iyeyo anati kwa ophun-
zira ake, 44 “Tamvetsetsani zimene ndikufuna kukuwuzani: Mwana wa
Munthu akupita kukaperekedwa m’manja mwa anthu.” 45 Koma iwo
sanazindikire zimene amatanthauza. Izi zinawadabwitsa kotero sanathe
kuzimvetsa ndipo anaopa kumufunsa.

### *Wamkulu Ndani?*

46 Mkangano unayambika pakati pa ophunzira wa kuti wamkulu koposa
akanakhala ndani mwa iwo. 47 Yesu podziwa maganizo awo, anatenga
kamwana nakayimika pambali pake. 48 Ndipo Iye anawawuza kuti,
“Aliyense wolandira bwino kamwana aka m’dzina langa, ndiye kuti
akulandiranso bwino Ine; ndipo aliyense wolandira bwino Ine, ndiye
kuti akulandiranso bwino amene ananditumа Ine. Pakuti amene ndi
wamng’ono pakati panu, ndiye amene ali wamkulu koposa.”

49 Yohane anati, “Ambuye, ife tinaona munthu akutulutsa ziwanda
m’dzina lanu ndipo tinayesa kumuletsa, chifukwa iyeyo si mmodzi wa
ife.”

50 Yesu anati, “Wosamuletsa, pakuti amene satsutsana nanu ali mbali
yanu.”

### *A Samariya Akana Yesu*

51 Nthawi itayandikira yoti Iye atengedwe kupita kumwamba, Yesu
anatsimikiza zopita ku Yerusalemu, 52 ndipo anatuma nthumwi kuti
zitsogole. Iwo anapita m’mudzi wa Asamariya kuti akonzekere kumu-
landira, 53 koma anthu kumeneko sanamulandire chifukwa Iye ankapita

ku Yerusalemu. [54] Ophunzira awa, Yohane ndi Yakobo ataona zimenezi,
anafunsa kuti, "Ambuye, kodi mukufuna ife tiyitane moto kuchokera
kumwamba kuti uwawononge?" [55] Koma Yesu anatembenuka ndi
kuwadzudzula, [56] ndipo iwo anapita ku mudzi wina.

### *Kutsatira Yesu*

[57] Pamene iwo ankayenda mu msewu, munthu wina anati kwa Iye, "Inu ndikutsatirani kulikonse kumene mudzapita."

[58] Yesu anayankha kuti, "Nkhandwe zili ndi mapanga ake, mbalame zili ndi zisa zake, koma Mwana wa Munthu alibe malo wogonekapo mutu wake."

[59] Iye anati kwa wina, "Nditsate Ine."

Koma munthuyo anayankha kuti, "Ambuye, choyamba loleni ndipite kuti ndikayike maliro a abambo anga."

[60] Yesu anati kwa iye, "Aleke akufa ayikane akufa okhaokha, koma iwe pita ukalalikire ufumu wa Mulungu."

[61] Koma winanso anati, "Ine ndidzakutsatani Ambuye; koma choyamba ndiloleni ndibwerere kuti ndikatsanzikane nalo banja langa."

[62] Yesu anayankha kuti, "Munthu amene akulima ndi khasu lokokedwa n'kumayang'ana m'mbuyo, si woyenera kugwira ntchito mu ufumu wa Mulungu."

## 10

### *Yesu Atuma Ophunzira 72*

[1] Zitatha izi Ambuye anasankha enanso 72 ndi kuwatumiza awiriawiri
patsogolo pake ku mzinda uliwonse ndi kumalo kumene Iye anatsala
pang'ono kupitako. [2] Iye anawawuza kuti, "Zokolola ndi zambiri, koma
ogwira ntchito ndi ochepa. Pemphani Ambuye wa zokolola, kuti atumize
antchito ku munda wake wa zokolola. [3] Pitani! Ine ndikukutumizani
ngati nkhosa pakati pa mimbulu. [4] Musatenge chikwama kapena thumba
kapena nsapato; ndipo musalonjere wina aliyense pa njira.

[5] "Mukamalowa m'nyumba, poyamba nenani kuti, 'Mtendere pa
nyumba ino.' [6] Ngati m'nyumbamo muli munthu wofuna mtendere,
mtendere wanuwo udzakhala pa iyeyo; ngati mulibemo, mtendere
wanuwo udzabwerera kwa inu. [7] Khalani m'nyumba yomweyo, idyani
ndi kumwa chilichonse chimene akupatsani, pakuti wantchito ayenera
kulandira malipiro ake. Musachoke kumene mwafikirako ndi kupita ku
nyumba zina.

[8] "Mukamalowa m'mudzi, ndi kulandiridwa, idyani chilichonse
akukonzerani. [9] Chiritsani odwala amene ali kumeneko ndipo muwawuze
kuti, 'Ufumu wa Mulungu wayandikira.' [10] Koma mukalowa m'mudzi
ndipo osalandiridwa bwino, kapiteni ku misewu m'mudzimo n'kukanena
kuti, [11] 'Tikukusansirani ngakhale fumbi la m'mudzi wanuwu limene
lamamatira ku mapazi athuwa. Komabe dziwani izi: Ufumu wa Mulungu
wayandikira.' [12] Ine ndikuwuzani kuti adzachita chifundo polanga
Sodomu pa tsikulo kusiyana ndi mudziwo.

[13] "Ndiwe watsoka, iwe Korazini! Ndiwe watsoka, iwe Betisaida!
Kukanakhala kuti zodabwitsa zimene zinachitika mwa inu zinachitika
ku Turo ndi Sidoni, iwo akanatembenuka mtima kale lomwe, atavala
ziguduli ndi kudzola phulusa. [14] Koma adzachita chifundo polanga Turo

ndi Sidoni kusiyana ndi inu. [15] Kodi iwe Kaperenawo, adzakukweza
mpaka kumwamba? Ayi, adzakutsitsa mpaka ku Malo a anthu akufa.

[16] "Womvera inu, akumvera Ine; wokana inu, akukana Ine. Ndipo
wokana Ine; akukana Iye amene ananditumа Ine."

[17] Anthu 72 aja anabwerera ndi chimwemwe ndipo anati, "Ambuye,
ngakhale ziwanda zinatigonjera ife m'dzina lanu."

[18] Iye anayankha kuti, "Ndinaona Satana akugwa kuchokera kumwamba
ngati mphenzi. [19] Ine ndakupatsani ulamuliro woponda njoka ndi
zinkhanira, ndi kugonjetsa mphamvu zonse za mdani; palibe chimene
chidzakupwetekani. [20] Komabe musakondwere chifukwa mizimu yoyipa
inakugonjerani, koma kondwerani chifukwa mayina anu analembedwa
kumwamba."

[21] Nthawi imeneyo Mzimu Woyera anadzaza Yesu ndi chimwemwe
ndipo anati, "Ine ndikulemekeza Inu, Atate Ambuye a kumwamba ndi
dziko lapansi, chifukwa mwawabisira anthu anzeru ndi ophunzira zinthu
izi ndipo mwaziwulula kwa ana aang'ono. Inde, Atate, pakuti munachita
zimenezi mwachifuniro chanu.

[22] "Atate anga anapereka zinthu zonse m'manja mwanga. Palibe
amene amadziwa Mwana kupatula Atate yekha, ndipo palibe amene
amadziwa Atate kupatula Mwana yekha, ndiponso amene Mwanayo
akufuna kumuwululira."

[23] Kenaka anatembenukira kwa ophunzira ake nawawuza iwo okha kuti,
"Ndi odala maso amene akuona zimene mukuonazi. [24] Pakuti kunena
zoona aneneri ambiri ndi mafumu anafunitsitsa kuona zimene mukuonazi
koma sanazione, ndi kumva zimene mukumvazi koma sanazimve."

### *Fanizo la Msamariya Wachifundo*

[25] Nthawi ina katswiri wa malamulo anayimirira kuti ayese Yesu. Iye
anati, "Aphunzitsi, ndichite chiyani kuti ndikhale ndi moyo wosatha?"

[26] Yesu anayankha kuti, "Mwalembedwa chiyani m'Malamulo, ndipo iwe
umawerenga zotani?"

[27] Iye anayankha kuti, "Uzikonda Yehova Mulungu wako ndi mtima
wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu zako zonse ndi nzeru
zako zonse, ndi kukonda mnansi wako monga iwe mwini."

[28] Yesu anayankha kuti, "Iwe wayankha bwino, chita zimenezi ndipo
udzakhala ndi moyo."

[29] Koma iye anafuna kudzilungamitsa yekha, ndipo anamufunsanso
Yesu kuti, "Kodi mnansi wanga ndani?"

[30] Yesu pomuyankha anati, "Munthu wina ankatsikira ku Yeriko
kuchokera ku Yerusalemu. Pa njira anavulazidwa ndi achifwamba.
Anamuvula zovala zake, namumenya ndi kuthawa, namusiya ali pafupi
kufa. [31] Wansembe ankapita pa njira yomweyo, ndipo ataona munthuyo,
analambalala. [32] Chimodzimodzinso, Mlevi wina pamene anafika pa
malopo ndi kumuona, analambalalanso. [33] Koma Msamariya wina, ali pa
ulendo wake, anafika pamene panali munthuyo; ndipo atamuona, anamva
naye chisoni. [34] Anapita panali munthu wovulalayo, nathira mafuta ndi
vinyo pa zilonda zake, n'kuzimanga. Kenaka anamukweza pa bulu wake,
napita naye ku nyumba ya alendo, namusamalira. [35] Mmawa mwake
anatenga ndalama ziwiri zasiliva nazipereka kwa woyang'anira nyum-
bayo, nati, 'Musamalireni munthuyu, ndipo pobwera ndidzakubwezerani
zonse zimene mugwiritse ntchito.'

36 “Kodi ukuganiza ndi ndani mwa atatuwa, amene anali mnansi wa
munthu amene anavulazidwa ndi achifwambawo?”
37 Katswiri wa Malamulo uja anayankha kuti, “Amene anamuchitira
chifundo.”
Yesu anamuwuza kuti, “Pita, uzikachita chimodzimodzi.”

### *Marita ndi Mariya*

38 Yesu ndi ophunzira ake akuyenda, anafika pa mudzi kumene mayi
wotchedwa Marita anamulandira Iye m’nyumba mwake. 39 Mayiyu anali
ndi mchemwali wake wotchedwa Mariya, amene anakhala pa mapazi a
Yesu kumverera zimene Iye ankanena. 40 Koma Marita anatanganidwa
ndi zokonzekera zonse zimene zimayenera kuchitika. Iye anabwera kwa
Yesu namufunsa kuti, “Ambuye, kodi simusamala kuti mchemwali wanga
wandisiya kuti ndichite ntchito yonse ndekha? Muwuzeni andithandize!”
41 Ambuye anati, “Marita, Marita, ukudandaula ndi kuvutika ndi zinthu
zambiri, 42 koma chofunika n’chimodzi chokha. Mariya wasankha chinthu
chabwino, ndipo palibe angamulande chimenechi.”

# 11

### *Yesu Aphunzitsa za ku Pemphera*

1 Tsiku lina Yesu amapemphera pamalo ena. Atamaliza, mmodzi wa
ophunzira ake anati kwa Iye, “Ambuye tiphunzitseni kupemphera, monga
momwe Yohane anaphunzitsira ophunzira ake.”
2 Yesu anawawuza kuti, “Pamene mukupemphera muzinena kuti:
“ ‘Atate,
dzina lanu lilemekezedwe,
ufumu wanu ubwere.
3 Mutipatse chakudya chathu chalero,
4 mutikhululukire machimo athu,
monga ifenso timakhululukira aliyense amene watilakwira.
Ndipo musalole kuti tigwe m’mayesero.’ ”
5 Kenaka anawawuza kuti, “Tiyerekeze: Mmodzi mwa inu atakhala
ndi bwenzi lake, ndipo iye n’kupita ku nyumba yake pakati pa usiku,
nakanena kuti, ‘Mnzanga, bwereke malofu atatu abuledi, 6 chifukwa
ndalandira bwenzi langa amene ali pa ulendo ndipo ine ndilibe choti
ndimupatse.’
7 “Ndipo yerekezani kuti amene ali m’nyumbamo ndi kuyankha kuti,
‘Usandivutitse ine, ndatseka kale chitseko, ndipo ine ndi ana anga tagona.
Ine sindingadzukenso kuti ndidzakupatse.’ 8 Ine ndikukuwuzani kuti
adzadzuka ndi kumupatsa bulediyo, osati chifukwa ndi bwenzi lake,
koma chifukwa cha liwuma la munthu wopemphayo, ndipo kudzamupatsa
zonse zimene akuzifuna.
9 “Choncho Ine ndikunena kwa inu kuti: Pemphani ndipo adzakupat-
sani. Funafunani ndipo mudzapeza. Gogodani ndipo adzakutsekulirani.
10 Pakuti aliyense amene amapempha amalandira. Munthu amene
amafunafuna amapeza. Iye amene amagogoda amamutsekulira.
11 “Ndani mwa inu abambo, kodi mwana wanu atapempha nsomba,
m’malo mwake mungamupatse njoka? 12 Kapena atapempha dzira, kodi
mungamupatse chinkhanira? 13 Tsono ngati inu, anthu oyipa, mumadziwa
kupereka mphatso zabwino kwa ana anu, koposa kotani Atate anu

akumwamba, angalephere bwanji kupereka Mzimu Woyera kwa amene
awapempha!"

### *Yesu ndi Belezebabu*

14 Yesu amatulutsa chiwanda chimene chinali chosayankhula. Chiwan-
dacho chitatuluka, munthu wosayankhulayo anayankhula, ndipo gulu la
anthu linadabwa. 15 Koma ena mwa iwo anati, "Iye akutulutsa ziwanda
ndi mphamvu ya Belezebabu mfumu ya ziwanda." 16 Ena anamuyesa
pomufunsa chizindikiro chochokera kumwamba.
17 Yesu anadziwa maganizo awo ndipo anawawuza kuti, "Ufumu
uliwonse wogawikana udzawonongeka, ndipo nyumba yogawikana idza-
pasuka. 18 Ngati Satana adziwukira yekha, ufumu wake ungalimbe
bwanji? Ine ndikunena izi chifukwa inu mukuti Ine ndimatulutsa ziwanda
ndi mphamvu ya Belezebabu. 19 Tsopano ngati Ine ndimatulutsa ziwanda
ndi mphamvu ya Belezebabu, nanga ophunzira anu amazitulutsa ndi
mphamvu ya ndani? Choncho, iwowo ndiye adzakhala oweruza anu.
20 Koma ngati ndimatulutsa ziwanda ndi mphamvu ya Mulungu, ndiye
kuti ufumu wa Mulungu wafika pakati panu.
21 "Munthu wamphamvu, amene ali ndi zida, akamalondera nyumba
yake, katundu wake amatetezedwa. 22 Koma pakabwera wina
wamphamvu zoposa namugonjetsa, amalanda zida zimene munthuyo
amazidalirazo ndi kugawa katundu wake.
23 "Munthu amene sali mbali yanga ndi wotsutsana nane. Ndipo
wosandithandiza kusonkhanitsa, ameneyo ndi womwaza.

### *Za Mzimu Woyipa*

24 "Mzimu woyipa ukatuluka mwa munthu, umakayendayenda ku
malo owuma, kufunafuna malo opumulirako ndipo suwapeza. Kenaka
umati, 'Ndibwerera ku nyumba kwanga kumene ndachokera.' 25 Ukafika
umapeza m'nyumba mosesedwa bwino ndi mokonza. 26 Pamenepo
umakatenga mizimu ina isanu ndi iwiri yoyipa kwambiri kuposa iwowo
ndipo imakalowa ndi kukhala m'menemo. Ndipo makhalidwe otsiriza a
munthuyo amakhala oyipa kuposa oyamba aja."

### *Munthu Wodala*

27 Pamene Yesu ankanena zonsezi, mayi wina m'gulu la anthuwo
anafuwula nati, "Ndi wodala amayi amene anakubalani ndi kukulerani!"
28 Koma Yesu anayankha kuti, "Odala ndi amene amamva mawu a
Mulungu ndi kuwasunga."

### *Chizindikiro cha Yona*

29 Pamene gulu la anthu limachuluka, Yesu anati, "Uno ndi m'bado
oyipa. Umafuna kuona chizindikiro chodabwitsa. Koma sadzachiona
kupatula chizindikiro chija cha Yona. 30 Monga Yona uja anali chizindikiro
kwa anthu ku Ninive, momwemonso Mwana wa Munthu adzakhala
chizindikiro kwa anthu a m'bado uno. 31 Mfumu yayikazi yakummwera
idzayimirira tsiku lachiweruzo pamodzi ndi anthu a m'bado uno ndipo
idzawatsutsa, chifukwa iyo inachokera kumapeto a dziko lapansi kudza-
mva nzeru za Solomoni. Ndipo tsopano pano pali wina woposa Solomoni.
32 Anthu a ku Ninive adzayimirira tsiku lachiweruzo pamodzi ndi m'bado
uno ndipo adzawutsutsa, pakuti anatembenuka mtima ndi ulaliki wa Yona.
Ndipo tsopano pano pali wina woposa Yona.

### *Nyale ndi Thupi*

33 "Palibe amene amayatsa nyale ndi kuyiika pa malo poti sionekera,
kapena pansi pa mtsuko. M'malo mwake amayika pa choyikapo chake,
kuti iwo amene akulowamo aone kuwunika. 34 Diso lanu ndi nyale ya
thupi lanu. Pamene maso anu ali bwino, thupi lanu lonse limadzaza ndi
kuwunika. Koma ngati ali oyipa, thupi lanunso ndi lodzaza ndi mdima.
35 Onetsetsani tsono, kuti kuwunika kuli mwa inu si mdima. 36 Choncho,
ngati thupi lanu lonse ndi lodzaza ndi kuwunika, ndiye kuti palibe dera
lina lili mdima, lonselo lidzakhala kuwunika, monga momwe kuwunika
kwa nyale kumakuwalirani."

### *Tsoka la Afarisi ndi Alembi Amalamulo*

37 Yesu atamaliza kuyankhula, Mfarisi wina anamuyitana kuti akadye
naye. Tsono Yesu analowa m'nyumba ndi kukhala podyera. 38 Mfarisiyo
anadabwa atazindikira kuti Yesu anayamba kudya wosatsata mwambo
wawo wakasambidwe ka m'manja.

39 Kenaka Ambuye anamuwuza kuti, "Inu Afarisi mumatsuka kunja kwa
chikho ndi mbale, koma m'kati mwanu ndi modzaza ndi kudzikonda ndi
zoyipa. 40 Anthu opusa inu! Kodi amene anapanga zam'kati sanapangenso
zakunja? 41 Koma popereka kwa osauka, perekani chimene chili m'kati
ndipo chilichonse chidzakhala choyera.

42 "Tsoka kwa inu Afarisi, chifukwa mumapereka kwa Mulungu chakhumi cha timbewu tonunkhira, ndi timbewu tokometsera chakudya ndi mbewu zina zonse za m'munda, koma mumakana chilungamo ndi chikondi cha Mulungu. Mumayenera kuchita zomalizirazi osalekanso kuchita zoyambazi.

43 "Tsoka kwa inu Afarisi, chifukwa mumakonda mipando yofunika kwambiri m'masunagoge ndi malonje m'malo a pa msika.

44 "Tsoka kwa inu Afarisi, chifukwa muli ngati manda osawaka, amene anthu amangoyendapo, osawadziwa."

45 Mmodzi mwa akatswiri a Malamulo anamuyankha Iye nati, "Aphunzitsi, pamene mukunena zinthu izi, mukutinyoza ifenso?"

46 Yesu anayankha kuti, "Tsoka kwa inunso akatswiri a Malamulo chifukwa mumawalemetsa anthu ndi mtolo umene iwo sangathe kunyamula, ndipo inu eni ake simutenga chala chanu kuti muwathandize.

47 "Tsoka kwa inu, chifukwa mumawaka manda a aneneri, komatu
ndi makolo anu amene anawapha. 48 Tsono potero mumachitira
umboni za zimene makolo anu anachita. Anapha aneneri, ndipo inu
mumawaka manda awo. 49 Chifukwa cha ichi, Mulungu mu nzeru
zake anati, 'Ine ndidzawatumizira aneneri ndi atumwi, ena mwa iwo
adzawapha ndipo ena adzawazunza.' 50 Choncho m'bado uwu udzasenza
magazi a aneneri onse amene anakhetsedwa kuyambira pachiyambi cha
dziko, 51 kuyambira magazi a Abele kufikira magazi a Zakariya amene
anaphedwa pakati pa guwa lansembe ndi malo opatulika. Inde, Ine
ndikuwuzani inu, m'bado uno udzasenza zonsezi.

52 "Tsoka kwa inu akatswiri a Malamulo, chifukwa mwachotsa kiyi wachidziwitso inu eni akenu musanalowemo, ndipo mwatsekerezanso iwo amene amalowa."

53 Pamene Yesu anachokamo, Afarisi ndi aphunzitsi a Malamulo
anayamba kumamutsutsa koopsa ndi kumupanikiza ndi mafunso,
54 pofuna kumukola muchina chilichonse chimene Iye angayankhule.

# 12

*Chenjezo ndi Chilimbikitso*

1 Nthawi yomweyo, anthu miyandamiyanda atasonkhana, ndi kumapon-
danapondana, Yesu anayamba kuyankhula poyamba kwa ophunzira
ake, nati, “Chenjereni ndi yisiti wa Afarisi, amene ndi chinyengo.
2 Palibe chinthu chophimbika chimene sichidzawululika, kapena chobisika
chimene sichidzadziwika. 3 Chimene mwanena mu mdima chidza-
mveka dzuwa likuwala, ndipo zimene mwanong’ona m’khutu m’chipinda
cham’kati, zidzayankhulidwa pa denga la nyumba.

4 “Ine ndikuwuzani, abwenzi anga, musachite mantha ndi amene
amapha thupi chifukwa akatero sangachitenso kanthu. 5 Koma Ine
ndidzakuonetsani amene muyenera kumuopa: Wopani Iye, amene pam-
buyo pakupha thupi, ali ndi mphamvu yakukuponyani ku gehena. Inde,
Ine ndikuwuzani, muopeni Iye. 6 Kodi atimba asanu samagulidwa ndi
ndalama ziwiri? Ngakhale zili chomwecho palibe imodzi ya izo imene
imayiwalika ndi Mulungu. 7 Ndithudi, tsitsi lonse la m’mutu mwanu
ndi lowerengedwa. Musachite mantha; inu ndi oposa kwambiri mpheta
zambiri.

8 “Ine ndikukuwuza kuti, aliyense amene avomereza Ine pamaso pa
anthu, Mwana wa Munthu adzamuvomerezanso pamaso pa angelo a Mu-
lungu. 9 Koma iye amene andikana Ine pamaso pa anthu adzakanidwanso
pamaso pa angelo a Mulungu. 10 Ndipo aliyense amene ayankhulira
Mwana wa Munthu mawu oyipa adzakhululukidwa, koma iye wochitira
mwano Mzimu Woyera sadzakhululukidwa.

11 “Akadzakutengerani ku masunagoge pamaso pa oweruza ndi a maula-
muliro, musadere nkhawa mmene mudzadzitchinjirizire nokha kapena
chimene mudzayankhule, 12 pakuti Mzimu Woyera nthawi imeneyo
adzakuphunzitsani zoyenera kunena.”

*Fanizo la Munthu Wachuma Wopusa*

13 Munthu wina m’gulu la anthu anati kwa Iye, “Aphunzitsi, muwuzeni
m’bale wanga andigawireko chuma chamasiye.”

14 Yesu anayankha kuti, “Munthu iwe, ndani anandiyika Ine kukhala
woweruza kapena wogawa chuma pakati panu?” 15 Kenaka Iye
anawawuza kuti, “Chenjerani! Khalani tcheru ndi makhalidwe onse
adyera; moyo wa munthu sukhala chifukwa cha kuchuluka kwa zimene
ali nazo.”

16 Ndipo Iye anawawuza fanizo ili, “Munda wa munthu wina wachuma
unabereka kwambiri. 17 Iye anaganiza kuti, ‘Ndichite chiyani? Ndilibe
malo osungiramo mbewu zanga.’

18 “Ndipo Iye anati, ichi ndi chimene ndidzachite: Ndidzaphwasula
nkhokwe zanga zonse ndi kumanga zokulirapo, ndipo ndidzasungira
m’menemo mbewu ndi katundu. 19 Ndipo ndidzawuza moyo wanga
kuti, ‘Uli nazo zinthu zabwino zambiri zimene zikhalepo zaka zambiri,
usapupulume; idya, imwa ndi kukondwera.’ ”

20 “Koma Mulungu anati kwa iye, ‘Iwe wopusa! Usiku womwe uno moyo
wako udzachotsedwa kwa iwe, ndipo ndi ndani amene adzatenge zimene
iwe wadzikonzera?’

21 “Umu ndi mmene zidzakhalire ndi aliyense amene amadziwunjikira
chuma, koma si wachuma pamaso pa Mulungu.”

*Musadere Nkhawa*

22 Kenaka Yesu anati kwa ophunzira ake, "Choncho Ine ndikuwuzani
kuti musadere nkhawa za moyo wanu, zimene mudzadya; kapena za
thupi lanu, zimene mudzavala. 23 Moyo uposa chakudya, ndi thupi
liposa chovala. 24 Taonani makwangwala: iwo safesa kapena kukolola,
alibe nyumba zosungamo zinthu kapena nkhokwe; komabe, Mulungu
amawadyetsa. Koposa kotani inu amene ndi ofunikira kuposa mbalame.
25 Ndi ndani wa inu akhoza kuwonjeza ora pa moyo wake chifukwa
cha kudandaula? 26 Popeza simungathe kuchita kanthu kakang'ono aka,
n'chifukwa chiyani mumadandaula ndi zinazi?
27 "Taonani mmene maluwa amakulira. Iwo sagwira ntchito kapena
kusoka zovala. Koma Ine ndikuwuzani kuti, ngakhale Solomoni
muulemelero wake wonse sanavalepo ngati limodzi la awa. 28 Ngati umu
ndi mmene Mulungu amavekera udzu wakuthengo, umene lero ulipo
ndipo mawa uponyedwa pa moto, nanga Iye adzakuvekani inu motani.
Haa! Inu achikhulupiriro chochepa! 29 Ndipo musayike mtima wanu pa
zimene mudzadye kapena kumwa; musade nazo nkhawa. 30 Pakuti anthu
akunja amathamanga kufunafuna zinthu zotere, ndipo Atate amadziwa
kuti mumazifuna zimenezi. 31 Koma funafunani ufumu wake, ndipo
mudzapatsidwa zonsezi.

### *Chuma cha Kumwamba*

32 "Musachite mantha, inu kagulu kankhosa, pakuti zinakondweretsa
Atate anu kuti akupatseni ufumu. 33 Gulitsani zonse zimene muli
nazo, ndipo ndalama zake mupereke kwa osauka. Dzipezereni zik-
wama zandalama zimene sizidzatha, ndi kudzikundikira chuma chomwe
sichidzatha kumwamba, kumene mbala sizingafikeko, ndipo dzimbiri
silingawononge. 34 Popeza kumene kuli chuma chanu, mtima wanunso
udzakhala komweko."

### *Kukhala a Atcheru*

35 "Khalani okonzekeratu ndipo nyale zanu ziziyaka, 36 ngati anthu
oyembekezera kubwera kwa mbuye wawo kuchokera kuphwando la
ukwati, kuti pamene afika ndi kugogoda akhoza nthawi yomweyo
kumutsekulira chitseko. 37 Zidzakhala bwino kwa antchitowo amene
mbuye wawo pobwera adzawapeze akudikira. Zoonadi, Ine ndikuwuzani
kuti adzakonzekera kuwatumikira, adzakhala nawo pa tebulo ndipo
adzabwera ndi kuwatumikira. 38 Zidzakhala bwino kwa antchitowo
amene mbuye wawo adzawapeze ali okonzeka, ngakhale iye atabwera pa
ora lachiwiri kapena lachitatu usiku. 39 Koma zindikirani izi: Ngati mwini
nyumba akanadziwa ora limene mbala ibwera, sakanalola kuti nyumba
yake ithyoledwe. 40 Inunso muyenera kukhala okonzeka, chifukwa Mwana
wa Munthu adzabwera pa ora limene simukumuyembekezera Iye."

### *Wantchito Wokhulupirika ndi Wosakhulupirika*

41 Petro anafunsa kuti, "Kodi mukunena fanizoli kwa ife, kapena kwa
aliyense?"
42 Ambuye anayankha kuti, "Kodi tsono woyang'anira wokhulupirika
ndi wanzeru ndani? Kodi ndi amene mbuye wake wamuyika kukhala
oyang'anira antchito ake kuti aziwapatsa ndalama yachakudya pa nthawi
yake yoyenera? 43 Zidzamukhalira bwino wantchito amene mbuye wake
adzamupeza akuchita zimene pamene iye abwera. 44 Zoonadi, Ine
ndikukuwuzani kuti adzamuyika kukhala woyang'anira katundu wake
yense. 45 Koma tiyerekeze kuti wantchitoyo aziganiza mu mtima mwake

kuti, ‘Bwana wanga akuchedwa kwambiri kubwera,’ ndipo kenaka ndi
kuyamba kumenya antchito aamuna ndi aakazi ndi kudya, kumwa ndi
kuledzera. 46 Mbuye wake adzabwera tsiku limene iye sakumuyembekez-
era ndi ora limene iye sakudziwa. Iye adzamulanga ndi kumusiya kumalo
kumene kuli osakhulupirira.
47 “Wantchito amene amadziwa chifuniro cha mbuye wake koma
wosakonzeka kapena wosachita chimene mbuye wake akufuna adzak-
wapulidwa zikwapu zambiri. 48 Koma wantchito amene sadziwa koma
n’kuchita zinthu zoyenera chilango, adzakwapulidwa zikwapu zochepa.
Aliyense amene anapatsidwa zambiri, adzayenera kubwezanso zambiri;
ndipo amene anamusungitsa zambiri, adzamulamula kuti abweze zam-
birinso.”

*Za Kugawikana*

49 “Ine ndabwera kudzayatsa moto pa dziko lapansi, ndipo
ndikanakonda ukanayaka kale. 50 Koma Ine ndiyenera kubatizidwa,
ndipo ndikusautsika mu mtima mpaka utachitika! 51 Kodi mukuganiza
kuti Ine ndinabwera kudzabweretsa mtendere pa dziko lapansi? Ayi,
Ine ndikukuwuzani kuti, ndinabweretsa kugawikana. 52 Kuyambira
tsopano mpaka m’tsogolo m’banja limodzi mudzakhala anthu asanu
ndipo adzawukirana wina ndi mnzake, atatu kuwukira awiri, ndipo
awiri kuwukira atatu. 53 Anthu adzawukirana. Abambo kudzawukira
mwana wawo wamwamuna, mwana wawoyo adzawukira abambo ake.
Amayi adzawukira mwana wawo wamkazi, mwana wawoyo adzawukira
amayi ake. Amayi adzawukira mpongozi wawo wamkazi, mpongoziyo
adzawukira amayiwo.”

*Kumasulira Nthawi*

54 Iye anati kwa gulu la anthu, “Pamene mukuona mtambo ukukwera
kummawa, nthawi yomweyo inu mumati, ‘kugwa mvula,’ ndipo imag-
wadi. 55 Ndipo pamene mphepo yakummwera ikuwomba, inu mumati
‘kutentha’ ndipo kumaterodi. 56 Achiphamaso inu! Inu mumadziwa
kutanthauzira maonekedwe a dziko lapansi ndi thambo. Zikutheka bwanji
kuti simukudziwa kumasulira kwa nthawi ino?
57 “Bwanji simukuzindikira nokha zoyenera kuchita? 58 Pamene
mukupita kwa woweruza ndi amene munalakwirana naye, yesetsani
kwambiri kuti muyanjane naye m’njiramo, chifukwa mukapanda kutero
akhoza kukutengerani ku bwalo la milandu ndipo woweruzayo adza-
kuperekani kwa woyang’anira ndende, ndipo woyang’anira ndendeyo
adzakuponyani m’ndende. 59 Ine ndikuwuzani kuti, simudzatulukamo
mpaka mutalipira ndalama zonse.”

# 13

*Za Kutembenuka Mtima*

1 Nthawi yomweyo panali ena amene analipo omwe amamuwuza Yesu
za Agalileya amene magazi awo Pilato anawasakaniza ndi nsembe zawo.
2 Yesu anayankha kuti, “Kodi mukuganiza kuti Agalileya amenewa anali
ochimwa kwambiri kuposa Agalileya ena onse chifukwa anavutika m’njira
iyi? 3 Ine ndikuti, ayi! Koma ngati inu simutembenuka mtima, inunso
mudzawonongeka nonse. 4 Kapena anthu 18 aja amene anafa nsanja
ya Siloamu itawagwera, kodi mukuganiza kuti iwo aja anali ochimwa
kwambiri kuposa onse amene amakhala mu Yerusalemu? 5 Ine ndikuti,

ayi! Koma ngati inu simutembenuka mtima, inunso mudzawonongeka nonse.”
6 Kenaka Iye anawawuza fanizo kuti, “Munthu wina anali ndi mtengo wamkuyu, umene anadzala m’munda wamphesa, ndipo Iye anapita kukayang’ana zipatso, koma sanazipeze.
7 Tsono kwa munthu amene amasamalira munda wamphesawo anati, ‘Kwa zaka zitatu tsopano ndakhala ndikubwera kudzafuna chipatso pa mtengo uwu ndipo sindinachipeze. Udule! N’chifukwa chiyani ukuwononga nthaka?’
8 “Munthuyo anayankha kuti, ‘Bwana, tawusiyani kwa chaka chimodzi chokha ndipo ine ndikumba ngalande mozungulira ndi kuthira manyowa.
9 Ngati udzabale zipatso chaka chamawa, zili bwino! Koma ngati sudzabala, pamenepo mudzawudule.’ ”

### *Mayi Wokhota Msana Achiritsidwa pa Sabata*

10 Pa Sabata Yesu ankaphunzitsa m’sunagoge ina,
11 ndipo momwemo munali mayi amene anali ndi mzimu woyipa umene unamudwalitsa zaka 18. Iye anali wokhota msana ndipo samatha kuweramuka ndi pang’ono pomwe.
12 Yesu atamuona anamuyitana kutsogolo ndipo anati kwa iye, “Amayi, mwamasulidwa ku mavuto.”
13 Kenaka anasanjika manja ake pa iye, ndipo nthawi yomweyo anawongoka nayamika Mulungu.
14 Chifukwa cha kuyipidwa kuti Yesu anachiritsa pa Sabata, wolamulira sunagoge anati kwa anthu, “Pali masiku asanu ndi limodzi ogwira ntchito. Choncho bwerani kuti mudzachiritsidwe masiku amenewo osati pa Sabata.”
15 Ambuye anamuyankha kuti, “Iwe wachiphamaso! Kodi nonsenu simumasula pa Sabata ng’ombe zanu kapena bulu kumuchotsa m’khola ndi kupita naye kukamupatsa madzi?
16 Nanga mayiyu, amene ndi mwana wa Abrahamu, ndipo anamangidwa ndi Satana zaka 18, kodi siwoyenera kuti amasulidwe msinga imeneyi pa tsiku la Sabata?”
17 Atanena izi, onse omutsutsa anachititsidwa manyazi, koma anthu anakondwera ndi zodabwitsa zonse zimene Iye anazichita.

### *Fanizo la Mbewu ya Mpiru ndi la Yisiti*

18 Kenaka Yesu anafunsa kuti, “Kodi ufumu wa Mulungu uli ngati chiyani? Kodi Ine ndingawufanizire ndi chiyani?
19 Uli ngati mbewu ya mpiru, imene munthu anatenga ndi kudzala m’munda mwake. Inakula, n’kukhala mtengo, ndipo mbalame zamlengalenga zinakhala m’nthambi zake.”
20 Iye anafunsanso kuti, “Kodi ufumu wa Mulungu ndingawufanizire ndi chiyani?
21 Uli ngati yisiti amene mayi anatenga ndi kusakaniza ndi ufa wambiri mpaka anafufumitsa ufawo.”

### *Khomo Lopapatiza*

22 Ndipo Yesu anayendayenda m’mizinda ndi m’midzi, kumaphunzitsa pamene Iye ankapita ku Yerusalemu.
23 Wina anamufunsa Iye kuti, “Ambuye, kodi ndi anthu ochepa okha amene adzapulumutsidwe?”
Iye anawawuza kuti,
24 “Yesetsani kulowa pa khomo lopapatiza, chifukwa ndikukuwuzani kuti ambiri adzafuna kulowa koma sadzatha kutero.
25 Nthawi yomwe mwini nyumba adzayimirira ndi kutseka chitseko, inu mudzayima kunja kugogoda ndi kudandaula kuti, ‘Bwana, tatitsekulirani khomo.’
“Koma Iye adzayankha kuti, ‘Ine sindikukudziwani ndipo sindikudziwanso kumene mwachokera.’

26 “Ndipo inu mudzati, tinkadya ndi kumwa ndi inu ndipo munkaphun-
zitsa m’misewu yathu.
27 “Koma Iye adzayankha kuti, ‘Ine sindikukudziwani ndipo sindikudzi-
wanso kumene mwachokera. Chokereni inu nonse ochita zoyipa!’
28 “Mudzalira ndi kukuta mano mukadzaona Abrahamu, Isake ndi
Yakobo ndi aneneri onse ali mu ufumu wa Mulungu koma inuyo
mutaponyedwa kunja. 29 Anthu adzachokera kummawa ndi kumadzulo,
kumpoto ndi kummwera, kudzakhala pa phwando mu ufumu wa
Mulungu. 30 Ndithudi otsirizira ndiye adzakhale oyambirira, ndipo
oyambirira ndiye adzakhale otsirizira.”

### *Yesu Amvera Chisoni Yerusalemu*

31 Pa nthawi imeneyo Afarisi anabwera kwa Yesu ndipo anati kwa Iye,
“Chokani malo ano ndipo pitani kumalo ena aliwonse. Herode akufuna
kukuphani.”
32 Iye anayankha kuti, “Pitani kawuzeni nkhandweyo, Ine ndikutulutsa
ziwanda ndi kuchiritsa anthu lero ndi mawa ndipo tsiku lachitatu
ndidzakwaniritsa cholinga changa.” 33 M’njira ina iliyonse, Ine ndiyenera
kupitirira ulendo wanga lero, mawa ndi mkuja. Zoona n’zakuti mneneri
sangafere kunja kwa Yerusalemu.
34 Iwe Yerusalemu, Yerusalemu! Umapha aneneri ndi kuwagenda
miyala anthu amene atumizidwa kwa iwe. Nthawi zambiri ndakhala
ndikufuna kusonkhanitsa ana ako pamodzi, monga nkhuku imasonkhan-
itsira anapiye pansi pa mapiko ake, koma iwe sunafune! 35 Taona, nyumba
yako yasanduka bwinja. Ine ndikukuwuza kuti, sudzandionanso mpaka
pamene udzati, “Wodala amene akubwera m’dzina la Ambuye!”

## 14

### *Yesu M’nyumba ya Mfarisi*

1 Pa tsiku lina la Sabata, Yesu atapita kukadya ku nyumba ya Mfarisi
wodziwika, Afarisi anamulonda mosamalitsa. 2 Poteropo, patsogolo pake
panali munthu amene anadwala matenda otupa mimba ndi miyendo.
3 Yesu anafunsa Afarisi ndi akatswiri amalamulo kuti, “Kodi ndi zololedwa
kuchiritsa pa tsiku la Sabata kapena ayi?” 4 Koma iwo sanayankhe. Tsono
atamutenga munthuyo, Iye anamuchiritsa ndipo anamuwuza kuti azipita.
5 Kenaka Iye anawafunsa kuti, “Kodi ngati mmodzi mwa inu ali ndi
mwana wamwamuna kapena ng’ombe imene yagwera m’chitsime tsiku la
Sabata, kodi simungamuvuwulemo tsiku lomwelo?” 6 Ndipo iwo analibe
choyankha.

### *Kudzichepetsa ndi Kulandira Ulemu*

7 Iye ataona momwe alendo amasankhira malo aulemu pa tebulo, Iye
anawawuza fanizo ili: 8 “Pamene wina wakuyitanani ku phwando la
ukwati, musakhale pa malo aulemu ayi, chifukwa mwina anayitananso
munthu wina wolemekezeka kuposa inu. 9 Ngati zitatero, ndiye kuti
munthu uja amene anakuyitani inu nonse awiri adzakuwuzani kuti,
‘Mupatseni munthu uyu malo anu.’ Pamenepo inu mudzachita manyazi,
pokakhala malo wotsika. 10 Koma akakuyitanani, khalani pa malo otsika,
kuti amene anakuyitanani uja adzakuwuzeni kuti, ‘Bwenzi, bwera udza-
khale pa malo aulemu pano.’ Pamenepo inu mudzalandira ulemu pamaso
pa alendo anzanu onse. 11 Pakuti aliyense wodzikuza adzamuchepetsa,
ndipo aliyense wodzichepetsa adzamukweza.”

12 Kenaka Yesu anati kwa mwini malo uja, “Ukakonza chakudya
chamasana kapena chamadzulo, usamayitane abwenzi ako, abale ako,
anthu afuko lako kapena anzako achuma; ngati iwe utero, iwo adzakuyi-
tananso, choncho udzalandiriratu mphotho yako. 13 Koma ukakonza ph-
wando, itana anthu osauka, ofa ziwalo, olumala ndi osaona. 14 Pamenepo
udzakhala wodala, chifukwa iwo sangakubwezere kanthu, koma Mulungu
ndiye adzakubwezera pa chiukitso cha olungama.”

### *Fanizo la Phwando Lalikulu*

15 Mmodzi mwa amene amadya naye atamva izi, anati kwa Yesu, “Ndi
wodala munthu amene adzadye nawo mu ufumu wa Mulungu.”

16 Yesu anayankha kuti, “Munthu wina ankakonza phwando lalikulu
ndipo anayitana alendo ambiri. 17 Nthawi yaphwando itakwana anatuma
wantchito wake kuti akawuze onse amene anayitanidwa kuti, ‘Bwerani,
pakuti zonse zakonzeka.’

18 “Koma onse anayamba kupereka zifukwa mofanana. Woyamba
anati, ‘Ine ndangogula kumene munda, ndipo ndikuyenera kupita kuti
ndikawuone. Pepani mundikhululukire.’

19 “Wina anati, ‘Ndangogula kumene ng’ombe khumi zokoka ngolo
ndipo kupita kukaziyesa. Pepani mundikhululukire.’

20 “Wina anatinso, ‘Ine ndangokwatira kumene, choncho sinditha
kubwera.’

21 “Wantchitoyo anabwera ndikudzamuwuza bwana wakeyo zimenezi.
Pamenepo mphwandoyo anapsa mtima ndipo analamula wantchito
wakeyo kuti, ‘Pita msangamsanga kunja m’misewu ndi m’makwalala a
mu mzinda ndipo ukabweretse osauka, ofa ziwalo, osaona ndi olumala.’

22 “Wantchitoyo anati, ‘Bwana, zimene munanena zachitika koma malo
akanalipobe.’

23 “Ndipo mbuye uja anawuza wantchito wake kuti, ‘Pita kunja ku
misewu ikuluikulu ndi kunja kwa mpanda ndipo ukawawuze kuti alowe,
kuti nyumba yanga idzaze. 24 Ine ndikukuwuzani inu kuti palibe ndi
mmodzi yemwe mwa anthu amene anayitanidwa adzalawa phwandolo.’ ”

### *Dipo la Kutsatira Yesu*

25 Gulu lalikulu la anthu linkayenda naye Yesu ndipo atatembenukira
kwa iwo anati, 26 “Ngati wina aliyense abwera kwa Ine ndipo sadana ndi
abambo ndi amayi ake, mkazi wake ndi ana, abale ake ndi alongo ake, inde
ngakhale moyo wake omwe, iye sangakhale ophunzira wanga. 27 Ndipo
aliyense amene sasenza mtanda wake ndi kunditsata Ine sangakhale
ophunzira wanga.

28 “Taganizani, ngati wina mwa inu akufuna kumanga nsanja, kodi iye
sayamba wakhala pansi ndi kuganizira za mtengo wake kuti aone ngati
ali ndi ndalama zokwanira kuti atsirizire? 29 Pakuti ngati ayika maziko
ndi kulephera kutsiriza, aliyense amene adzayiona adzamuseka, 30 nanena
kuti, ‘Munthu uyu anayamba kumanga koma sanathe kutsiriza.’

31 “Kapena mfumu imene ikupita ku nkhondo kukamenyana ndi mfumu
ina, kodi siyamba yakhala pansi ndi kulingalira ngati ingathe ndi anthu
10,000 kulimbana ndi amene akubwera ndi 20,000? 32 Ngati singathe,
idzatuma nthumwi pomwe winayo ali kutali ndi kukapempha mgwirizano
wamtendere. 33 M’njira yomweyo, wina aliyense wa inu amene sasiya
zonse ali nazo sangakhale ophunzira wanga.

34 “Mchere ndi wabwino, koma ngati usukuluka adzawukoleretsanso ndi
chiyani? 35 Suyeneranso ngakhale m’nthaka kapena kudzala la manyowa;
umatayidwa kunja.
“Amene ali ndi makutu akumva, amve.”

# 15

### *Fanizo la Nkhosa Yotayika*

1 Tsopano amisonkho ndi “ochimwa” ankasonkhana kudzamvera mawu
ake. 2 Koma Afarisi ndi aphunzitsi amalamulo amang’ung’udza nati,
“Munthu uyu amalandira ochimwa ndi kudya nawo.”
3 Ndipo Yesu anawawuza fanizo ili: 4 “Tiyerekeze kuti mmodzi mwa
inu ali ndi nkhosa 100 ndipo imodzi yatayika, kodi iye sangasiye 99
zija kutchire ndi kupita kukafuna yotayikayo mpaka atayipeza? 5 Ndipo
iye akayipeza, amayinyamula pa phewa lake mwachimwemwe 6 ndi
kupita kwawo. Kenaka amayitana anzake ndi anansi pamodzi, ndi
kuti, ‘Kondwerani nane; ine ndayipeza nkhosa yanga yotayika ija.’
7 Ine ndikukuwuzani kuti momwemonso kudzakhala chikondwerero
chachikulu kumwamba chifukwa cha wochimwa mmodzi amene watem-
benuka mtima kusiyana ndi anthu olungama 99 amene ali otembenuka
mtima kale.”

### *Fanizo la Ndalama Yotayika*

8 “Kapena tiyeni tifanizire mayi amene anali ndi ndalama zasiliva khumi
ndipo imodzi n’kutayika, kodi sayatsa nyale ndi kusesa m’nyumba ndi
kufuna mosamalitsa mpaka atayipeza? 9 Ndipo pamene wayipeza, amay-
itana anzake, ndi anansi pamodzi nati, ‘Kondwerani nane; ine ndayipeza
ndalama yanga yotayika ija.’ 10 Momwemonso, Ine ndikukuwuzani kuti
angelo a Mulungu amakondwera kwambiri chifukwa cha wochimwa
mmodzi amene watembenuka mtima.”

### *Fanizo la Mwana Wolowerera*

11 Yesu anapitiriza kunena kuti, “Panali munthu amene anali ndi ana
aamuna awiri. 12 Wamng’onoyo anati kwa abambo ake, ‘Abambo, patseni
gawo langa la chuma chanu.’ Ndipo iye anawagawira awiriwo chuma
chawo.
13 “Pasanapite nthawi, wamng’onoyo anasonkhanitsa chuma chake
chonse, napita ku dziko lakutali ndipo kumeneko anayamba kumwaza
chuma chake m’njira zachitayiko. 14 Iye atawononga zonse, kunagwa
njala yoopsa m’dziko lonselo ndipo anayamba kusauka. 15 Iye anapita
kwa nzika ina ya dzikolo nakakhala naye ndi kumagwira ntchito, amene
anamutumiza ku munda kukadyetsa nkhumba. 16 Iye analakalaka
atakhutitsa mimba yake ndi makoko amene nkhumbazo zinkadya, koma
panalibe wina amene anamupatsa kanthu.
17 “Maganizo ake atabweramo, iye anati, ‘Ndi antchito angati a abambo
anga amene ali ndi chakudya chimene amadya n’kutsalako ndipo ine ndili
pano kufa ndi njala! 18 Ine ndinyamuka ndi kubwerera kwa abambo
anga ndipo ndikati kwa iwo: abambo, ine ndachimwira kumwamba ndi
kwa inu. 19 Ndine wosayeneranso kutchedwa mwana wanu; munditenge
ngati mmodzi wa antchito anu.’ 20 Ndipo iye ananyamuka ndi kupita kwa
abambo ake.
“Koma iye akanali patali, abambo ake anamuona ndipo anamvera
chisoni; anathamangira mwanayo, namukumbatira ndi kupsompsona.

21 “Mwanayo anati, ‘Abambo, ine ndachimwira kumwamba ndi inunso.
Ine sindiyenera konse kutchedwa mwana wanu.’
22 “Koma abambowo anati kwa antchito ake, ‘Fulumirani! Bweretsani
mkanjo wabwino kwambiri ndipo mumuveke. Muvekeni mphete ndi
nsapato. 23 Bweretsani mwana wang’ombe wonenepa ndipo iphani.
Tiyeni tikhale ndi phwando ndi kukondwerera. 24 Pakuti mwana wangayu
anali wakufa, ndipo ali ndi moyonso; iye anatayika ndipo wapezeka.’
Chomwecho anayamba kukondwerera.
25 “Nthawi imeneyi, mwana wake wamkulu uja anali ku munda. Iye
atafika pafupi ndi nyumba, anamva anthu akuyimba ndi kuvina. 26 Ndipo
iye anayitana mmodzi wa antchito, namufunsa chimene chimachitika.
27 Iye anayankha kuti, ‘M’bale wako wabwera ndipo abambo ako apha
mwana wang’ombe wonenepa chifukwa wabwera wamoyo ndipo ali
bwino.’
28 “Mwana wamkulu anakwiya ndipo anakana kulowa. Chomwecho
abambo ake anatuluka ndi kumudandaulira. 29 Koma iye anayankha
abambo ake kuti, ‘Taonani! Zaka zonsezi ndakhala ndikukutumikirani
kugwira ntchito yowawa ndipo palibe pamene sindinamvere malamulo
anu. Koma inu simunandipatse ngakhale mwana wambuzi kuti ine
ndichite phwando ndi anzanga. 30 Koma pamene mwana wanu uyu amene
wawononga chuma chanu ndi achiwerewere wabwera ku nyumba, inu
mwamuphera mwana wang’ombe wonenepa.’ ”
31 Abambowo anati, “Mwana wanga, iwe umakhala ndi ine nthawi
zonse ndipo zonse ndili nazo ndi zako. 32 Koma tinayenera kukondwera
ndi kusangalala, chifukwa m’bale wako uyu anali wakufa ndipo ali ndi
moyonso; iye anali wotayika ndipo wapezeka.”

# 16

*Fanizo la Kapitawo Wosakhulupirika*

1 Yesu anawuza ophunzira ake kuti, “Panali munthu wina wachuma
amene kapitawo wake anzake anamuneneza kuti amawononga chuma
chakecho. 2 Choncho anamuyitana ndi kumufunsa kuti, ‘Kodi n’chiyani
chimene ndikumva za iwe? Pereka tsatanetsatane wa ntchito yako, pakuti
supitirizanso kukhala kapitawo wanga.’
3 “Kapitawoyo analingalira kuti, ‘Kodi tsopano ndidzachita chiyani?
Bwana wanga andichotsa ntchito. Ine ndilibe mphamvu zokwanira
zolimira, komanso ine ndimachita manyazi kupempha. 4 Ine ndikudziwa
chimene ndidzachita kotero kuti, pamene ntchito yanga yatha pano, anthu
adzandilandire m’nyumba zawo.’
5 “Choncho iye anayitana aliyense amene anali ndi ngongole kwa bwana
wake. Iye anafunsa woyamba, ‘Kodi uli ndi ngongole yotani kwa bwana
wanga?’
6 “Iye anayankha kuti, ‘Migolo yamafuta a olivi 800.’
“Kapitawo uja anamuwuza iye, ‘Tenga pamene unalemba ngongole
yakoyo, khala pansi msanga ndipo lemba kuti ndi migolo 400.’
7 “Kenaka iye anafunsa wachiwiri kuti, ‘Nanga iwe uli ndi ngongole
yotani?’
“Iye ayankha kuti madengu a tirigu 1,000.
“Iye anati, ‘Tenga pamene unalemba ngongole yakoyo ndipo ulembepo
800.’

8 “Bwana anayamikira kapitawo wosakhulupirikayo popeza anachita
mochenjera. Pakuti anthu a dziko lino lapansi ndi ochenjera kwambiri
akamachita zinthu ndi anthu ofanana nawo kuposa anthu a kuwunika.
9 Ine ndikukuwuzani inu, gwiritsani ntchito chuma cha dziko lapansi
kuti mudzipezere nokha abwenzi, kuti pamene chatha mudzalandiridwe
m’malo okhala amuyaya.

10 “Amene akhulupirika pa zinthu zochepa akhoza kukhulupirikanso
pa zinthu zambiri, ndipo amene sakhulupirika pa zinthu zochepa
adzakhala wosakhulupirika pa zinthu zambiri. 11 Ndipo ngati simu-
nakhale okhulupirika pogwiritsa ntchito chuma cha dziko lapansi, ndani
amene adzakusungitsani chuma chenicheni? 12 Ndipo ngati simunakhale
okhulupirika ndi chuma cha mwini wake, ndani amene adzakupatsani
katundu wanuwanu?

13 “Palibe wantchito amene angatumikire mabwana awiri. Mwina iye
adzadana ndi wina ndi kukonda winayo, kapena adzakhala wodzipereka
kwa wina ndi kumunyoza winayo. Inu simungathe kutumikira Mulungu
komanso ndalama nthawi imodzi.”

14 Afarisi amene ankakonda ndalama atamva zimenezi anamuseka Yesu.
15 Yesu anawawuza kuti, “Inu ndi amene mumadzilungamitsa nokha
pamaso pa anthu, koma Mulungu amadziwa mitima yanu. Zinthu zimene
anthu amaziyesa zopambana, ndi zonyansa pamaso pa Mulungu.

### *Ziphunzitso Zina*

16 “Malamulo ndi Aneneri zinagwira ntchito mpaka nthawi ya Yohane.
Kuyambira nthawi imeneyo, Uthenga Wabwino wa ufumu wa Mulungu
ukulalikidwa, ndipo aliyense akuyesetsa mwamphamvu kuti alowemo.
17 N’kwapafupi kuti kumwamba ndi dziko lapansi zichoke kulekana ndi
kuti kalemba kakang’ono kachoke m’Malamulo.

18 “Aliyense amene asiya mkazi wake ndi kukakwatira mkazi wina
akuchita chigololo, ndipo mwamuna amene akwatira mkazi wosiyidwayo
akuchitanso chigololo.”

### *Za Munthu Wachuma ndi Lazaro*

19 “Panali munthu wachuma amene ankavala zovala zofiirira za mten-
gowapatali ndipo ankakhala moyo wachisangalalo tsiku lililonse. 20 Pa
khomo la mpanda wake ankagonekapo munthu wopempha wotchedwa
Lazaro, wazilonda thupi lonse 21 ndipo ankafunitsitsa atadya zomwe
zinkagwa pansi kuchokera pamene munthu wolemerayo amadyerapo.
Agalu ankabweranso ndi kumanyambita zilonda zake.

22 “Nthawi inafika imene wopemphayo anamwalira ndipo angelo ana-
munyamula nakamuyika m’manja mwa Abrahamu. Munthu wolemerayo
anamwaliranso ndipo anayikidwa m’manda. 23 Ali m’gehena kuzunzika,
anakweza maso ake ndipo anaona Abrahamu ali ndi Lazaro pambali
pake. 24 Ndipo anafuwula kwa iye kuti, ‘Abambo Abrahamu, mundimvere
chisoni ine ndipo mutumeni Lazaroyo kuti aviyike msonga ya chala chake
m’madzi kuti aziziritse lilime langa, chifukwa ndikumva ululu m’moto
muno.’

25 “Koma Abrahamu anayankha kuti, ‘Mwanawe kumbukira kuti nthawi
yamoyo wako unalandira zinthu zako zabwino, pamene Lazaro analandira
zinthu zoyipa, koma tsopano akusangalatsidwa kuno ndipo iwe uli
m’mazunzo. 26 Ndipo kuwonjezera pa zonsezi, pakati pa inu ndi ife
pali chiphompho chachikulu chimene chinayikidwa, kotero kuti amene

akufuna kubwera kumeneko sangathe, kapena palibe amene angawoloke
kuchokera kumeneko kudzafika kuno.'
27 "Iye anayankha kuti, 'Ndipo ndikupemphani inu, abambo, mutumeni
Lazaro ku nyumba ya abambo anga, 28 pakuti ine ndili ndi abale
asanu. Lolani iye akawachenjeze kotero kuti asadzabwere kumalo ano
amazunzo.'
29 "Abrahamu anayankha kuti, 'Ali ndi Mose ndi Aneneri; aleke amvere
iwo.'
30 "Iye anati, 'Ayi, bambo Abrahamu, koma ngati wina ochokera kwa
akufa adzapita kwa iwo, adzatembenuka mtima.'
31 "Anati kwa iye, 'Ngati iwo samvera Mose ndi Aneneri, sadza-
khulupirira ngakhale wina atauka kwa akufa.' "

# 17

*Za Uchimo, Chikhulupiriro ndi Ntchito*

1 Yesu anati kwa ophunzira ake, "Zinthu zimene zimachimwitsa
sizingalephere kubwera, koma tsoka kwa munthu wozibweretsayo.
2 Kukanakhala bwino kwa iye kuti aponyedwe m'nyanja atamangiririridwa
mwala wamphero m'khosi mwake kusiyana kuti achimwitse mmodzi
mwa ana aang'onowa. 3 N'chifukwa chake dziyang'anireni nokha.
"Ngati m'bale wanu achimwa, mudzudzuleni, ndipo ngati alapa,
mukhululukireni. 4 Ngati iye akulakwira kasanu ndi kawiri pa tsiku,
ndipo ngati n'kubweranso kwa iwe kasanu ndi kawiri nati, 'Ndalapa,'
umukhululukire."
5 Atumwiwo anati kwa Ambuye, "Kulitsani chikhulupiriro chathu!"
6 Yesu anayankha kuti, "Ngati muli ndi chikhulupiriro chaching'ono
ngati kambewu kampiru, mukhoza kulamula mtengo wamkuyu uwu kuti,
'Zulidwa ndi kukadzalidwa m'nyanja,' ndipo udzakumverani.
7 "Tiyerekeze kuti mmodzi mwa inu anali ndi wantchito wolima kapena
woweta nkhosa, kodi angawuze wantchitoyo atabwera ku munda kuti,
'Tsopano bwera kuno khala pansi kuti udye?' 8 Kodi sangamuwuze
kuti, 'Konzere chakudya cha madzulo, iweyo ukonzeke ndipo undidikirire
pamene ndikudya ndi kumwa; kenaka ukhoza kudya ndi kumwa?' 9 Kodi
iye angathokoze wantchitoyo chifukwa chochita chimene anawuzidwa ku-
chita? 10 Chimodzimodzi inunso, mukachita zonse zimene munawuzidwa,
muzinena kuti, 'Ndife antchito osayenera; tangogwira ntchito yathu
basi.' "

*Yesu Achiritsa Akhate Khumi*

11 Tsopano Yesu anayenda m'malire a pakati pa Samariya ndi Galileya pa
ulendo wake wa ku Yerusalemu. 12 Akulowa m'mudzi wina, amuna khumi
amene anali ndi khate anakumana naye. Iwo anayima patali 13 ndipo
anafuwula ndi mawu okweza kuti, "Yesu, Ambuye, tichitireni chifundo!"
14 Iye atawaona, anati, "Pitani kadzionetseni nokha kwa ansembe."
Ndipo pamene iwo ankapita, anachiritsidwa.
15 Mmodzi wa iwo, ataona kuti wachiritsidwa, anabwerera, nayamika
Mulungu ndi mawu okweza. 16 Anagwetsa nkhope yake nagwa pa mapazi
a Yesu ndi kumuthokoza. Ndipo iye anali Msamariya.
17 Yesu anafunsa kuti, "Kodi amene anachiritsidwa sanalipo khumi?
Nanga asanu ndi anayi ena ali kuti? 18 Kodi palibe mmodzi mwa
iwo amene anabwerera kudzalemekeza Mulungu kupatula mlendoyu?"

19 Pamenepo anati kwa iye, “Imirira ndipo pita; chikhulupiriro chako chakuchiritsa iwe.”

### *Za Ufumu wa Mulungu*

20 Ndipo Afarisi atamufunsa Iye kuti, ufumu wa Mulungu udzabwera
liti, Yesu anayankha kuti, “Mulungu sakhazikitsa ufumu wake mooneka
ndi maso, 21 kapenanso kuti anthu adzati, ‘Uwu uli apa,’ kapena ‘Uwo uli
apo,’ Pakuti taonani ufumu wa Mulungu uli pakati panu.”
22 Kenaka Iye anati kwa ophunzira ake, “Masiku akubwera pamene inu
mudzalakalaka mutaona tsiku limodzi la masiku a Mwana wa Munthu,
koma simudzaliona. 23 Anthu adzakuwuzani kuti, ‘Uyo ali apoyo!’ kapena
‘Uyu ali apa!’ Musawathamangire iwo. 24 Pakuti monga mphenzi
ing’anima ndi kuwala kuchokera mbali ina ya thambo kufikira inzake,
koteronso adzakhala ali Mwana wa Munthu pa tsiku lake. 25 Koma
poyamba ayenera kuzunzika mu zambiri ndi kukanidwa ndi m’bado uno.
26 “Monga mmene zinkachitikira nthawi ya Nowa, momwemonso
zidzachitikanso nthawi ya Mwana wa Munthu. 27 Anthu ankadya, kumwa,
kukwatira ndi kukwatiwa mpaka tsiku limene Nowa analowa m’chombo.
Pomwepo chigumula chinafika ndi kuwawononga onsewo.
28 “Zinalinso chimodzimodzi nthawi ya Loti. Anthu ankadya ndi kumwa,
kugula ndi kugulitsa, kudzala ndi kumanga. 29 Koma tsiku limene
Loti anachoka ku Sodomu, moto ndi sulufule zinavumbwa kuchokera
kumwamba ndi kuwawononga onsewo.
30 “Zidzakhalanso choncho Mwana wa Munthu akadzaonekera. 31 Tsiku
limenelo munthu amene ali pa denga la nyumba yake, ndi katundu wake
ali m’nyumbamo, asadzatsike kukatenga. Chimodzimodzinso, munthu
amene adzakhale ali ku munda asadzabwerere kukatenga chilichonse.
32 Kumbukirani mkazi wa Loti! 33 Aliyense amene ayesetsa kusunga
moyo wake adzawutaya, ndipo aliyense amene ataya moyo wake adza-
wusunga. 34 Ine ndikukuwuzani inu, usiku umenewo anthu awiri adzag-
ona pa mphasa imodzi; wina adzatengedwa ndipo wina adzasiyidwa.
35 Amayi awiri adzakhala pamodzi akusinja; wina adzatengedwa ndi
wina adzasiyidwa. 36 Amuna awiri adzakhala akulima m’munda; wina
adzatengedwa ndi wina adzasiyidwa.”
37 Iwo anafunsa kuti, “Ambuye, kodi zimenezi zidzachitikira kuti?”
Iye anayankha kuti, “Kumene kuli mtembo, n’kumene makwangwala amasonkhanako.”

# 18

### *Fanizo la Mayi Wakhama pa Kupempha*

1 Kenaka Yesu anawuza ophunzira ake fanizo kuwaonetsa kuti iwo
ayenera kumapemphera nthawi zonse ndikuti asafowoke. 2 Iye anati,
“M’mudzi wina munali woweruza wosaopa Mulungu ngakhalenso kula-
badira za anthu. 3 Ndipo panali mkazi wamasiye m’mudzimo amene
ankabwerabwera kwa iye ndi dandawulo lake kuti, ‘Mundiweruze mlandu
mwachilungamo pakati pa ine ndi otsutsana nane.’
4 “Kwa nthawi yayitali woweruzayo ankakana. Koma pa mapeto
analingalira nati, ‘Ngakhale kuti sindiopa Mulungu kapena kulabadira
za anthu, 5 koma chifukwa chakuti mkazi wamasiyeyu akundivutitsa,
ine ndimuweruzira mlandu wake mwachilungamo kuti asanditopetse ndi kubwerabwera kwakeko!’ ”

6 Ndipo Ambuye anati, "Tamvani zimene woweruza wopanda chilung-
amoyu wanena. 7 Tsono chingamuletse n'chiyani Mulungu kubweretsa
chilungamo kwa osankhika ake, amene amalira kwa Iye usana ndi
usiku? Kodi adzapitirirabe osawalabadira? 8 Ine ndikukuwuzani inu,
adzaonetsetsa kuti alandire chilungamo, ndiponso mofulumira. Komabe,
pamene Mwana wa Munthu akubwera, kodi adzapeza chikhulupiriro pa
dziko lapansi?"

### *Fanizo la Mfarisi ndi Wolandira Msonkho*

9 Yesu ananena fanizoli kwa amene amadzikhulupirira mwa iwo okha
kuti anali wolungama nanyoza ena onse. 10 "Anthu awiri anapita ku
Nyumba ya Mulungu kukapemphera, wina Mfarisi ndi winayo wolandira
msonkho. 11 Mfarisiyo anayimirira ndipo anapemphera za iye mwini kuti,
'Mulungu, ine ndikuyamika kuti sindili ngati anthu ena onse, achifwamba,
ochita zoyipa, achigololo, sindilinso ngati wolandira msonkhoyu. 12 Ine
ndimasala kudya kawiri pa Sabata ndipo ndimapereka chakhumi pa zonse
ndimapeza.'

13 "Koma wolandira msonkhoyo ali chiyimire potero, sanathe n'komwe
kuyang'ana kumwamba; koma anadziguguda pachifuwa ndipo anati,
'Mulungu, chitireni chifundo, ine wochimwa.'

14 "Ine ndikukuwuzani kuti munthu wolandira msonkhoyu, osati
Mfarisiyu, anapita kwawo atalungamitsidwa pamaso pa Mulungu. Chi-
fukwa chake, aliyense wodzikweza adzachepetsedwa, ndipo wodzichep-
etsa adzakwezedwa."

### *Yesu Adalitsa Ana Aang'ono*

15 Anthu amabweretsanso ana aang'ono kwa Yesu kuti awadalitse.
Ophunzira ataona izi, anawadzudzula. 16 Koma Yesu anayitana anawo
kuti abwere kwa Iye nati, "Lolani ana abwere kwa Ine ndipo musawat-
sekereze, pakuti ufumu wa Mulungu uli wa anthu otere. 17 Zoonadi, Ine
ndikukuwuzani kuti aliyense amene salandira ufumu wa Mulungu ngati
mwana wamng'ono, sadzalowamo."

### *Munthu Wachuma ndi Ufumu wa Mulungu*

18 Oweruza wina wake anamufunsa Iye kuti, "Aphunzitsi abwino,
ndichite chiyani kuti ndilandire moyo wosatha?"

19 Yesu anamuyankha kuti, "Chifukwa chiyani ukunditcha wabwino,
palibe wabwino kupatula Mulungu yekha. 20 Iwe umadziwa malamulo:
'Usachite chigololo, usaphe, usabe, usapereke umboni wonama, lemekeza
abambo ndi amayi ako.' "

21 Iye anati, "Zonsezi ndinasunga kuyambira ndili mnyamata."

22 Yesu atamva izi, anati kwa iye, "Ukusowabe chinthu chimodzi: Gulitsa
zonse zimene uli nazo ndipo uzipereke kwa osauka, ndipo udzakhala ndi
chuma kumwamba. Kenaka ubwere, nunditsate ine."

23 Atamva zimenezi, anakhumudwa kwambiri chifukwa anali munthu
wachuma chambiri. 24 Yesu anamuyang'ana nati, "N'kwapatali kwambiri
kuti anthu achuma akalowe mu ufumu wa Mulungu! 25 Ndithudi,
n'kwapafupi kuti ngamira idutse pa kabowo ka zingano kusiyana ndi
munthu wachuma kulowa mu ufumu wa Mulungu."

26 Amene anamva izi anafunsa kuti, "Nanga ndani amene angapulu-
muke?"

27 Yesu anayankha kuti, “Zinthu zosatheka ndi anthu zimatheka ndi
Mulungu.”

28 Petro anati kwa Iye, “Ife tinasiya zonse tinali nazo kutsatira Inu!”

29 Yesu anawawuza kuti, “Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti palibe
amene anasiya nyumba kapena mkazi kapena abale kapena makolo
kapena ana chifukwa cha ufumu wa Mulungu 30 adzalephera kulandira
mowirikiza m’moyo uno, ndi m’moyo ukubwerawo, moyo wosatha.”

### *Yesu Aneneratu za Imfa Yake Kachitatu*

31 Yesu anatengera khumi ndi awiriwo pambali ndi kuwawuza kuti,
“Taonani ife tikupita ku Yerusalemu, ndipo zonse zimene zalembedwa ndi
Aneneri za Mwana wa Munthu zidzakwaniritsidwa. 32 Iye adzaperekedwa
kwa anthu a mitundu ina. Ndipo adzamuchita chipongwe, adzamunyoza,
adzamulavulira, 33 adzamukwapula ndi kumupha. Tsiku lachitatu Iye
adzaukanso.”

34 Ophunzira sanazindikire china chilichonse cha izi. Tanthauzo lake
linabisika kwa iwo, ndipo sanadziwe chimene Iye amayankhula.

### *Yesu Achiritsa Wosaona*

35 Yesu atayandikira ku Yeriko, munthu wina wosaona amene amakhala
pambali pa msewu namapempha, 36 anamva gulu la anthu likudutsa. Iye
anafunsa chomwe chimachitika. 37 Iwo anamuwuza kuti “Yesu wa ku
Nazareti akudutsa.”

38 Iye anayitana mofuwula, “Yesu Mwana wa Davide, mundichitire
chifundo!”

39 Iwo amene amamutsogolera njira anamudzudzula ndi kumuwuza
kuti akhale chete, koma iye anafuwulabe, “Mwana wa Davide, chitireni
chifundo!”

40 Yesu anayima nalamula kuti abwere naye kwa Iye. Atabwera pafupi,
Yesu anamufunsa kuti, 41 “Kodi ukufuna kuti ndikuchitire chiyani?”

Iye anayankha kuti, “Ambuye, ine ndifuna ndionenso.”

42 Yesu anati kwa iye, “Onanso; chikhulupiriro chako chakupulumutsa.”
43 Nthawi yomweyo anaonanso ndipo anayamba kumutsatira Yesu, akule-
mekeza Mulungu. Anthu onse ataona izi, iwonso analemekeza Mulungu.

# 19

### *Zakeyu Apulumutsidwa*

1 Yesu analowa mu Yeriko napitirira. 2 Kunali munthu kumeneko
dzina lake Zakeyu; iye anali mkulu wa wolandira msonkho ndipo anali
wolemera. 3 Iye ankafuna kuona Yesu kuti ndani, koma pokhala wamfupi
sanathe chifukwa cha gulu la anthu. 4 Choncho iye anathamangira
patsogolo ndipo anakwera mu mtengo wamkuyu kuti amuone Iye, pakuti
Yesu ankadutsa njira imeneyo.

5 Yesu atafika pa malopo, anayang’ana mmwamba ndipo anati kwa
iye, “Zakeyu, tsika msangamsanga. Ine ndiyenera kukhala m’nyumba
mwako lero.” 6 Ndipo nthawi yomweyo anatsika ndipo anamulandira
mosangalala.

7 Anthu onse ataona zimenezi anayamba kung’ung’udza, nati, “Iye
akupita kuti akakhale mlendo wa wochimwa.”

8 Koma Zakeyu anayimirira ndipo anati kwa Ambuye, "Taonani Ambuye! Theka la chuma changa ndipereka kwa osauka ndipo ngati ndinamubera wina aliyense pa chilichonse, ndidzamubwezera mochulukitsa kanayi."
9 Yesu anati kwa iye, "Lero chipulumutso chafika m'nyumba ino, chifukwa munthu uyu nayenso ndi mwana wa Abrahamu. 10 Pajatu Mwana
wa Munthu anabwera kudzafunafuna ndi kupulumutsa chotayikacho."

### *Antchito Opindula Mosiyana*

11 Pamene iwo ankamvera izi, Iye anapitiriza kuwawuza fanizo, chifukwa Iye anali kufupi ndi Yerusalemu ndipo anthu ankaganiza kuti
ufumu wa Mulungu ukanaoneka nthawi yomweyo. 12 Iye anati, "Munthu
wa banja laufumu anapita ku dziko lakutali kukadzozedwa ufumu ndipo
kenaka abwerenso kwawo. 13 Tsono iye anayitana antchito ake khumi
ndi kuwapatsa ndalama khumi. Iye anati, 'Gwiritsani ntchito ndalama izi mpaka nditabwerera.'
14 "Koma anthu ake anamuda ndipo anatuma nthumwi pambuyo pake kukanena kuti, 'Sitikufuna munthuyu kuti akhale mfumu yathu.'
15 "Iye analandira ufumuwo ngakhale zinali zotero, ndipo anabwerera kwawo. Kenaka iye anatumiza uthenga kwa antchito ake amene anawapatsa ndalama aja, ndi cholinga chakuti adziwe chimene anapindula nazo.
16 "Woyamba anabwera ndipo anati, 'Bwana ndalama zanu zapindula khumi zina.'
17 "Bwana wakeyo anayankha kuti, Wachita bwino wantchito wabwino. 'Chifukwa wakhulupirika pa zinthu zazing'ono, lamulira mizinda khumi.'
18 "Wachiwiri anabwera ndipo anati, 'Bwana, ndalama zanu zapindula zisanu zina.'
19 "Bwana anayankha kuti, 'Iwe lamulira mizinda isanu.'
20 "Kenaka wantchito wina anabwera ndipo anati, 'Bwana, ndalama
yanu nayi; ine ndinayibisa ndi kuyisunga m'kansalu. 21 Ine ndimakuopani,
chifukwa ndinu munthu wowuma mtima. Inu mumatenga chimene simunachiyike ndi kukolola chimene simunadzale.'
22 "Bwana wake anayankha kuti, 'Ine ndikukuweruza iwe ndi mawu ako omwewo. Ndiwe wantchito woyipa. Kani umadziwa kuti ndine munthu wowuma mtima ndi wotenga chimene sindinasungitse, ndi kukolola
chimene sindinadzale? 23 Nanga n'chifukwa chiyani sunasungitse ndalama yanga, kuti ine pobwera, ndidzayitenge ndi chiwongoladzanja?'
24 "Ndipo iye anawuza amene anayimirira pafupi kuti, 'Tengani ndalama yake ndi kumupatsa amene ali ndi ndalama khumiyo!' "
25 Iwo anati, "Bwana iyeyu ali nazo kale khumi!"
26 Iye anayankha kuti, "Ndikukuwuzani kuti, aliyense amene ali nazo, adzapatsidwa zambiri, koma amene alibe, adzalandidwa ngakhale
chimene ali nacho. 27 Tsono adani anga aja amene sankafuna kuti ndikhale
mfumu yawo, abweretseni pano ndi kuwapha ine ndikuona."

### *Yesu Alowa mu Yerusalemu Mwaulemerero*

28 Yesu atatha kunena izi, anayendabe kupita ku Yerusalemu. 29 Iye
atayandikira ku Betifage ndi Betaniya pa phiri lotchedwa Olivi, Iye
anatuma awiri a ophunzira nati kwa iwo, 30 "Pitani m'mudzi uli patsogolo panu, mukakalowa m'mudzimo, mukapeza mwana wabulu womangiririridwa amene wina aliyense sanakwerepo. Mukamumasule
ndi kubwera naye kuno. 31 Ngati wina aliyense akakufunsani kuti,

'N'chifukwa chiyani mukumumasula mwana buluyo?' Mukamuwuze kuti,
'Ambuye akumufuna.' "
32 Otumidwawo anapita nakamupeza mwana wabulu monga momwe
Yesu anawawuzira. 33 Pamene ankamasula mwana wabuluyo, eni ake
anawafunsa kuti, "N'chifukwa chiyani mukumasula mwana wabuluyo?"
34 Iwo anayankha kuti, "Ambuye akumufuna."
35 Iwo anabweretsa buluyo kwa Yesu, naponya zovala zawo pa bulupo
ndi kumukwezapo Yesu. 36 Pamene ankapita, anthu anayala zovala zawo
mu msewu.
37 Iye atafika pafupi ndi pamene msewu umatsikira ku phiri la Olivi,
gulu lonse la ophunzira linayamba kuyamika Mulungu mwachimwemwe
ndi mawu ofuwula chifukwa cha zodabwitsa zonse anaziona.
38 "Yodala mfumu imene ikubwera m'dzina la Ambuye!"

"Mtendere kumwamba ndi ulemerero mmwambamwamba!"
39 Ena mwa Afarisi m'gulumo anati kwa Yesu, "Aphunzitsi, adzudzuleni
ophunzira anu!"
40 Iye anayankha kuti, "Ine ndikukuwuzani kuti, ngati atakhala chete,
miyala idzafuwula."
41 Iye atayandikira ku Yerusalemu ndi kuona mzindawo, anawulirira
42 nati, "Iwe ukanadziwa lero lino zinthu zokubweretsera mtendere, koma
tsopano zabisikira maso ako. 43 Pakuti masiku adzabwera pamene adani
ako adzamanga mitumbira yankhondo nakuzungulira, nadzakutsekereza
mbali zonse. 44 Iwo adzakugwetsera pansi, iwe, ana ako onse a m'kati
mwako. Iwo sadzasiya mwa iwe mwala wina pa unzake, chifukwa
sunazindikire nthawi ya kubwera kwa Mulungu."

### *Yesu m'Nyumba ya Mulungu*

45 Kenaka Iye analowa m'dera la Nyumba ya Mulungu ndi kuyamba
kutulutsa kunja amene amachita malonda. 46 Iye anawawuza kuti,
"Zinalembedwa kuti Nyumba yanga idzakhala nyumba ya mapemphero,
koma inu mwayisadutsa phanga la achifwamba."
47 Tsiku lililonse amaphunzitsa m'Nyumba ya Mulungu. Koma akulu
a ansembe, aphunzitsi amalamulo ndi atsogoleri pakati pa anthu
amayesetsa kuti amuphe. 48 Komabe iwo sanathe kupeza njira ina iliyonse
kuti achite izi, chifukwa anthu onse anakhulupirira mawu ake.

## 20

### *Amufunsa Yesu za Ulamuliro Wake*

1 Tsiku lina pamene Iye ankaphunzitsa anthu m'mabwalo a Nyumba
ya Mulungu ndi kuphunzitsa Uthenga Wabwino, akulu a ansembe ndi
aphunzitsi amalamulo, pamodzi ndi akuluakulu anabwera kwa Iye.
2 Iwo anati, "Mutiwuze mukuchita izi ndi ulamuliro wayani? Ndani
anakupatsani ulamuliro uwu?"
3 Iye anayankha kuti, "Inenso ndikufunsani, mundiyankhe, 4 'Kodi
ubatizo wa Yohane, unali wochokera kumwamba, kapena wochokera kwa
anthu?' "
5 Iwo anakambirana pakati pawo ndikuti, "Ngati ife tinena kuti,
'Kuchokera kumwamba' Iye akatifunsa kuti, 'chifukwa chiyani simuna-
mukhulupirire iye?' 6 Koma ngati ife tinena kuti, 'kuchokera kwa anthu,'

anthu onse atigenda miyala, chifukwa amatsimikiza kuti Yohane anali mneneri.”
7 Pamenepo iwo anayankha kuti, “Ife sitidziwa kumene unachokera.”
8 Yesu anati, “Ngakhale Inenso sindikuwuzani kuti ndi ulamuliro wanji umene ndikuchitira zimenezi.”

### *Fanizo la Olima M'munda Wamphesa*

9 Iye anapitirira kuwawuza anthu fanizo ili: “Munthu wina analima munda wamphesa, nabwereketsa kwa alimi ena ndipo anachoka kwa
nthawi yayitali.
10 Pa nthawi yokolola, iye anatumiza wantchito wake kwa alimi aja kuti amupatseko zina mwa zipatso za munda wamphesawo. Koma alimi aja anamumenya namubweza wopanda kanthu.
11 Iye anatumiza wantchito wina, koma uyunso anamumenya namuchita
zachipongwe ndi kumubweza wopanda kanthu.
12 Iye anatumizanso wina wachitatu ndipo iwo anamuvulaza namuponya kunja.
13 “Kenaka mwini mundawo anati, ‘Kodi ndichite chiyani? Ndidzatumiza mwana wanga wamwamuna, amene ndimukonda; mwina iwo adzamuchitira ulemu.’
14 “Koma alimiwo ataona mwanayo, anakambirananso. Iwo anati, ‘Uyu ndiye wodzamusiyira chumachi. Tiyeni timuphe ndipo chumachi chikhala
chathu.’
15 Ndipo anamuponya kunja kwa mundawo ndi kumupha.
“Nanga tsono mwini munda wamphesayo adzawatani anthuwa?
16 Iye adzabwera ndi kupha alimi aja ndi kupereka mundawo kwa ena.”
Pamene anthu anamva izi, anati, “Musatero ayi.”
17 Yesu anawayang'anitsitsa ndipo anafunsa kuti, “Kodi tanthauzo lake ndi chiyani la zimene zinalembedwa kuti,

“ ‘Mwala umene omanga nyumba anawukana
wasanduka mwala wa pa ngodya.

18 Aliyense amene agwa pa mwalawu adzapweteka, koma iye amene udzamugwera udzamuphwanya.’ ”
19 Aphunzitsi amalamulo ndi akulu a ansembe amafuna njira yoti amuphe nthawi yomweyo, chifukwa anadziwa kuti ananena fanizo ili powatsutsa iwo. Koma iwo anali ndi mantha chifukwa cha anthu.

### *Za Kupereka Msonkho kwa Kaisara*

20 Pamene ankamulondalonda Iye, iwo anatumiza akazitape amene amaoneka ngati achilungamo. Iwo ankafuna kumutapa m'kamwa Yesu mu china chilichonse chimene Iye ananena kuti amupereke Iye kwa amene anali ndi mphamvu ndi ulamuliro oweruza.
21 Potero akazitapewo anamufunsa Iye kuti, “Aphunzitsi, tidziwa kuti mumayankhula ndi kuphunzitsa zimene zili zoonadi, ndi kuti simuonetsa tsankho koma mumaphunzitsa njira ya Mulungu mwachoonadi.
22 Kodi ndi bwino kwa ife kumapereka msonkho kwa Kaisara kapena kusapereka?”
23 Iye anaona chinyengo chawo ndipo anawawuza kuti,
24 “Onetseni ndalama. Chithunzi ndi malembawa ndi zayani?”
25 Iwo anayankha kuti, “Za Kaisara.”
Iye anawawuza kuti, “Ndiye perekani kwa Kaisara zake za Kaisara ndi kwa Mulungu zimene ndi za Mulungu.”
26 Iwo analephera kumupeza cholakwa pa zimene ankayankhula pamaso pa anthu. Ndipo pothedwa nzeru ndi yankho lake, iwo anakhala chete.

### *Za Kuuka kwa Akufa ndi Ukwati*

27 Ena mwa Asaduki, amene ankanena kuti kulibe kuuka kwa akufa,
anabwera kwa Yesu ndi funso. 28 Iwo anati, "Aphunzitsi, Mose anatilem-
bera kuti munthu akamwalira ndi kusiya mkazi wopanda ana, m'bale wa
munthu womwalirayo akuyenera kukwatira mkaziyo kuti amuberekere
ana m'bale wakeyo. 29 Tsopano panali abale asanu ndi awiri. Woyambayo
anakwatira mkazi ndipo anafa wopanda mwana. 30 Wachiwiri 31 ndipo
kenaka wachitatuyo anamukwatira iye, ndipo chimodzimodzi asanu ndi
awiri aja anafa osasiya ana. 32 Pa mapeto pake mkaziyo anafanso.
33 Tsopano, pa nthawi ya kuukanso, kodi mkaziyu adzakhala wayani
popeza onse asanu ndi awiri anamukwatirapo?"

34 Yesu anayankha kuti, "Anthu a m'bado uno amakwatira ndi kuk-
watiwa. 35 Koma m'moyo umene ukubwerawo, anthu amene adzaukit-
sidwe kwa akufa sadzakwatira kapena kukwatiwa. 36 Ndipo sadzafanso,
pakuti adzakhala ngati angelo. Iwo ndi ana a Mulungu, chifukwa
adzakhala ataukitsidwa kwa akufa. 37 Ngakhale pa nkhani yachitsamba
choyaka moto, Mose anaonetsa kuti akufa amauka, pakuti anatcha
Ambuye 'Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake ndi Mulungu wa
Yakobo.' 38 Mulungu si Mulungu wa akufa, koma wa amoyo, pakuti kwa
Iye onse ali ndi moyo."

39 Ena mwa aphunzitsi amalamulo anayankha kuti, "Mwanena bwino
mphunzitsi!" 40 Ndipo panalibe wina amene akanalimba mtima kumu-
funsa Iye mafunso ena.

### *Khristu ndi Mwana wa Ndani?*

41 Kenaka Yesu anawawuza kuti, "Zikutheka bwanji kuti aziti Khristu
ndi mwana wa Davide? 42 Davide mwini wake akunenetsa m'buku la
Masalimo kuti,
"Ambuye anati kwa Ambuye anga:
'Khalani ku dzanja langa lamanja,
43 mpaka Ine nditasandutsa adani anu
chopondapo mapazi anu?'
44 Davide akumutcha Iye 'Ambuye.' Nanga zingatheke bwanji kuti Iye
akhale mwana wake?"

### *Achenjeza za Aphunzitsi Amalamulo*

45 Pamene anthu onse ankamvetsera, Yesu anati kwa ophunzira ake,
46 "Chenjerani ndi aphunzitsi amalamulo. Iwo amakonda kuyenda
atavala mikanjo ndipo amakonda kulonjeredwa m'misika ndipo amakhala
m'mipando yofunika m'masunagoge ndi m'malo aulemu m'maphwando.
47 Amawadyera akazi amasiye chuma chawo ndi kuchita mapemphero
aatali kuti awaone. Anthu oterewa adzalangidwa kwambiri."

## 21

### *Chopereka cha Mayi Wamasiye*

1 Yesu atayang'ana, anaona olemera akuyika mphatso zawo mu
chosungira ndalama za m'Nyumba ya Mulungu. 2 Iye anaonanso mkazi
wamasiye wosauka akuyikamo timakopala tiwiri. 3 Iye anati, "Zoonadi,
Ine ndikukuwuzani kuti mkazi wamasiye wosaukayu wapereka zambiri
kuposa ena onsewa. 4 Anthu onsewa atapa mphatso zawo kuchokera pa
zochuluka zimene ali nazo; koma uyu, mwa umphawi wake, wapereka
zonse zimene ali nazo."

*Zizindikiro za Masiku Otsiriza*

5 Ena mwa ophunzira ake ankachita ndemanga za mmene Nyumba ya
Mulungu anayikongoletsera ndi miyala yokongola ndiponso zinthu zina
zomwe anthu anapereka kwa Mulungu. Koma Yesu anati, 6 "Koma zimene
mukuziona panozi, nthawi idzafika pamene ngakhale mwala umodzi
omwe sudzakhala pa unzake; uliwonse udzagwetsedwa pansi."

7 Iwo anafunsa kuti, "Aphunzitsi, kodi zonsezi zidzachitika liti? Ndipo
tidzaonera chiyani kuti zili pafupi kuchitika?"

8 Iye anayankha kuti, "Chenjerani kuti musanyengedwe. Pakuti ambiri
adzabwera m'dzina langa nadzati 'Ine ndine Iye' ndi kuti 'Nthawi
yayandikira.' Musadzawatsate iwo. 9 Mukadzamva zankhondo ndi
zipolowe, musadzachite mantha. Zinthu izi ziyenera kuchitika poyamba,
koma chimaliziro sichidzafika nthawi yomweyo."

10 Kenaka anawawuza kuti, "Mtundu wa anthu udzawukirana ndi
mtundu wina, ndi ufumu kuwukira ufumu wina. 11 Kudzakhala
zivomerezi zazikulu, njala ndi miliri m'malo osiyanasiyana, ndi zinthu
zoopsa ndi zizindikiro zamphamvu kuchokera kumwamba.

12 "Koma zonsezi zisanachitike, adzakugwirani ndi kukuzunzani. Adza-
kuperekani ku masunagoge ndi ku ndende, ndipo adzakutengerani
pamaso pa mafumu ndi olamulira, ndipo zonsezi zidzachitika chifukwa
cha dzina langa. 13 Umenewu udzakhala mwayi wanu ochitira umboni.
14 Koma tsimikizani mtima kuti musadzade nkhawa za momwe mudzadz-
itchinjirizire. 15 Pakuti Ine ndidzakupatsani mawu ndi nzeru kotero kuti
palibe mmodzi wa adani anu adzathe kuwakana kapena kuwatsutsa.
16 Inu mudzaperekedwa ndi makolo anu, abale, anansi ndi abwenzi anu
ndipo ena mwa inu adzakuphani. 17 Anthu onse adzakudani chifukwa
cha Ine. 18 Koma palibe tsitsi limodzi la m'mutu mwanu lidzawonongeke.
19 Mukadzalimbikira ndiye mudzapeze moyo.

*Kuwonongedwa kwa Yerusalemu*

20 "Mukadzaona Yerusalemu atazingidwa ndi magulu ankhondo, inu
mudzadziwe kuti kuwonongeka kwake kuli pafupi. 21 Pamenepo amene ali
ku Yudeya adzathawire ku mapiri, amene ali mu mzinda adzatulukemo,
ndi amene ali ku midzi asadzalowe mu mzinda. 22 Pakuti iyi ndi nthawi
yachilango pokwaniritsa zonse zimene zinalembedwa. 23 Zidzakhala
zoopsa nthawi imenewo kwa amayi oyembekezera ndi amayi oyamwitsa!
Kudzakhala masautso aakulu m'dziko ndipo anthu onse adzawakwiyira.
24 Iwo adzaphedwa ndi lupanga ndi kutengedwa ukapolo kupita ku mayiko
wonse. Yerusalemu adzaponderezedwa ndi anthu a mitundu ina mpaka
nthawi ya a mitundu ina itakwaniritsidwa.

25 "Padzakhala zizindikiro zodabwitsa pa dzuwa, mwezi ndi nyenyezi.
Pa dziko lapansi, mitundu ya anthu idzakhala m'masautso ndipo idza-
thedwa nzeru pakumva mkokomo ndi mafunde a m'nyanja. 26 Anthu
adzakomoka chifukwa cha mantha, akadzamva za zimene zikubw-
era pa dziko lapansi, pakuti zinthu zamlengalenga zidzagwedezeka.
27 Nthawi imeneyo adzaona Mwana wa Munthu akubwera ndi mitambo,
mphamvu ndi ulemerero waukulu. 28 Zinthu izi zikadzayamba kuchitika,
mudzayimirire ndi kutukula mitu yanu, chifukwa chipulumutso chanu
chayandikira."

*Fanizo la Mtengo Wamkuyu*

[29] Iye anawawuza fanizo ili, "Taonani mtengo wamkuyu ndi mitengo
ina yonse. [30] Ikamatulutsa masamba, mumakhoza kudzionera nokha ndi
kudziwa kuti dzinja lili pafupi. [31] Chimodzimodzinso, mukadzaona zinthu
zonsezi, dziwani kuti ufumu wa Mulungu uli pafupi.
[32] "Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti m'bado uno sudzatha mpaka
zinthu zonsezi zitachitika. [33] Kumwamba ndi dziko lapansi zidzatha, koma
mawu anga sadzatha."

### *Za Kukhala Tcheru*

[34] "Samalani, kuti mitima yanu ingalemetsedwe ndi maphwando,
kuledzera ndi kudera nkhawa za moyo uno, ndi kuti tsiku ilo lingadzaku-
pezeni modzidzimutsa ngati msampha. [35] Pakuti lidzafika pa onse okhala
pa dziko lonse lapansi. [36] Khalani tcheru nthawi zonse ndi kupemphera
kuti inu mudzathe kuthawa zonse zimene zili pafupi kuchitika, ndi kuti
mudzathe kuyima pamaso pa Mwana wa Munthu."
[37] Tsiku lililonse Yesu amaphunzitsa ku Nyumba ya Mulungu, ndi
madzulo ali wonse Iye amachoka kukakhala pa phiri la Olivi usiku wonse.
[38] Ndipo anthu onse amabwera mmamawa kudzamumva Iye ku Nyumba
ya Mulungu.

# 22

### *Yudasi Avomera Kumupereka Yesu*

[1] Phwando la buledi wopanda yisiti lotchedwa Paska litayandikira,
[2] akulu a ansembe ndi aphunzitsi amalamulo amafunafuna mpata woti
amuphere Yesu, pakuti ankachita mantha ndi anthu. [3] Kenaka Satana
analowa mwa Yudasi, wotchedwa Isikarioti, mmodzi wa khumi ndi
a iwiriwo. [4] Ndipo Yudasi anapita kwa akulu a ansembe ndi akulu
oyang'anira Nyumba ya Mulungu ndi kukambirana nawo za mmene iye
angaperekere Yesu. [5] Iwo anakondwa ndipo anagwirizana zomupatsa
ndalama. [6] Iye anavomera, ndipo anayamba kufunafuna mpata wabwino
wakuti amupereke Yesu kwa iwo pamene panalibe gulu la anthu pafupi.

### *Paska Womaliza*

[7] Kenaka linafika tsiku la buledi wopanda yisiti pamene mwana
wankhosa wa Paska amaperekedwa nsembe. [8] Yesu anatuma Petro ndi
Yohane nati, "Pitani kukatikonzera Paska kuti tikadye."
[9] Iwo anafunsa kuti, "Kodi mukufuna tikakonzere kuti?"
[10] Iye anayankha kuti, "Taonani, mukamalowa mu mzinda, mudza-
kumana ndi mwamuna atanyamula mtsuko wamadzi. Mulondoleni ku
nyumba imene akalowe, [11] ndipo mukamuwuze mwini nyumbayo kuti,
'Aphunzitsi kufunsa kuti, chili kuti chipinda cha alendo, kumene Ine
ndi ophunzira anga tikadyere Paska?' [12] Iyeyo adzakuonetsani chipinda
chachikulu chapamwamba, chokhala ndi zonse. Kachiteni zokonzekera
m'menemo."
[13] Iwo anapita nakapeza zinthu monga mmene Yesu anawawuzira.
Tsono anakonza Paska.

### *Za Mgonero wa Ambuye*

[14] Ora litakwana, Yesu ndi ophunzira ake anakhala pa tebulo. [15] Ndipo
Iye anawawuza kuti, "Ine ndakhala ndikuyembekezera kudya Paska
uyu ndi inu ndisanamve zowawa. [16] Pakuti Ine ndikukuwuzani kuti

sindidzadyanso Paska wina mpaka Paskayi itakwaniritsidwa mu ufumu wa Mulungu."

17 Atanyamula chikho, Iye anayamika ndipo anati, "Tengani ndipo pat-
siranani pakati panu. 18 Pakuti ndikukuwuzani kuti, Ine sindidzamwanso
zochokera ku chipatso cha mphesa mpaka ufumu wa Mulungu utabwera."

19 Ndipo Iye anatenga buledi, nayamika ndipo anamunyema, nagawira iwo nati, "Ili ndi thupi langa lomwe laperekedwa kwa inu; muzichita zimenezi pokumbukira Ine."

20 Chimodzimodzinso, utatha mgonero, anatenga chikho nati, "Chikho
ichi ndi pangano latsopano la magazi anga, amene akhetsedwa chifukwa
cha inu. 21 Koma dzanja la amene akundipereka Ine lili pamodzi
ndi langa pa chakudya pano. 22 Mwana wa Munthu apita monga
mmene zinalembedwera, koma tsoka kwa munthu amene amupereka
Iye." 23 Iwo anayamba kufunsana pakati pawo kuti ndi ndani wa iwo
amene akanachita ichi.

### *Mkangano Pakati pa Ophunzira*

24 Komanso mkangano unabuka pakati pawo kuti ndani mwa iwo amene
amaganiziridwa kukhala wamkulu. 25 Yesu anawawuza kuti, "Mafumu a
anthu a mitundu ina amaonetsa mphamvu za ufumu wawo pa anthuwo;
ndipo amene ali ndi ulamuliro, amapatsidwa dzina la kuti 'Opindula.'
26 Koma inu simuyenera kukhala choncho. M'malo mwake, wamkulu
pakati panu akhale ngati wamng'ono pa onse, ndipo iye amene alamulira
akhale ngati wotumikira. 27 Pakuti wamkulu ndani, iye amene ali pa
tebulo kapena iye amene akutumikira? Kodi si iye amene ali pa tebulo?
Koma ndili pakati panu ngati mmodzi wokutumikirani. 28 Inu ndinu
amene mwayima nane m'mayesero. 29 Ndipo Ine ndikupatsani inu ufumu,
monga momwe Atate anga anandipatsiranso Ine, 30 kuti inu muthe kudya
ndi kumwa pa tebulo langa mu ufumu wanga ndi kukhala pa mipando
yaufumu kuweruza mafuko khumi ndi awiri a Israeli."

### *Yesu Aneneratu kuti Petro Adzamukana*

31 "Simoni, Simoni, Satana wapempha kuti akupete ngati tirigu. 32 Koma
Ine ndakupempherera Simoni, kuti chikhulupiriro chako chisafowoke
ndipo pamene udzabwerera kwa Ine, udzalimbikitse abale ako."

33 Koma iye anayankha kuti, "Ambuye, ndine wokonzeka kupita nanu ku ndende ndi kufa komwe."

34 Yesu anayankha kuti, "Ine ndikukuwuza Petro, tambala asanalire lero lino, udzandikana katatu kuti sukundidziwa Ine."

35 Kenaka Yesu anawafunsa iwo kuti, "Ine nditakutumizani wopanda chikwama cha ndalama, thumba kapena nsapato, kodi inu munasowa kanthu?"

Iwo anayankha kuti, "Palibe chimene tinasowa."

36 Iye anawawuza kuti, "Koma tsopano ngati muli ndi chikwama cha
ndalama, chitengeni, ndiponso thumba. Ndipo ngati mulibe lupanga,
gulitsani mkanjo wanu ndi kugula. 37 Zalembedwa kuti, 'Ndipo Iye
anawerengedwa pamodzi ndi anthu ochimwa,' ndipo Ine ndikuwuzani
kuti izi ziyenera kukwaniritsidwa mwa Ine. Inde, zimene zinalembedwa
za Ine, zikukwaniritsidwa."

38 Ophunzira anati, "Taonani Ambuye, awa malupanga awiri."

Iye anayankha kuti, "Amenewa akwanira."

### *Yesu Apemphera ku Phiri la Olivi*

39 Yesu anapitanso monga mwa masiku onse ku Phiri la Olivi, ndipo
ophunzira ake anamutsatira Iye. 40 Atafika pamalopo, Iye anawawuza
kuti, “Pempherani kuti musagwe m’mayesero.” 41 Iye anapita patsogolo
pang’ono patali ngati kuponya mwala, anagwada napephera kuti, 42 “Atate
ngati mukufuna chotsereni chikho ichi. Komatu muchite zimene muku-
funa osati zimene ndikufuna ine.” 43 Mngelo wochokera kumwamba
anafika namulimbikitsa. 44 Ndipo mopsinjika mtima, anapemphera
moona mtima, ndipo thukuta lake linali ngati madontho a magazi
akugwera pansi.

45 Iye atamaliza kupemphera, ndi kubwerera kwa ophunzira ake,
anawapeza atagona atafowoka ndi chisoni. 46 Iye anafunsa kuti,
N’chifukwa chiyani mukugona? “Dzukani ndipo pempherani kuti inu
musagwe m’mayesero.”

### *Amugwira Yesu*

47 Pamene Iye ankayankhulabe, gulu la anthu linabwera, ndipo munthu
wotchedwa Yudasi, mmodzi wa khumi ndi awiriwo analitsogolera. Iye
anamuyandikira Yesu kuti amupsompsone. 48 Koma Yesu anamufunsa
kuti, “Yudasi, kodi ukupereka Mwana wa Munthu ndi mpsopsono?”

49 Otsatira Yesu ataona zimene zimati zichitike, anati, “Ambuye, kodi
timenyane ndi malupanga athu?” 50 Ndipo mmodzi wa iwo anatema
wantchito wamkulu wa ansembe, nadula khutu lake lamanja.

51 Koma Yesu anayankha kuti, “Zisachitikenso zimenezi!” Ndipo Iye
anakhudza khutu la munthuyo ndi kumuchiritsa.

52 Kenaka Yesu anafunsa akulu a ansembe, akuluakulu oyang’anira
Nyumba ya Mulungu ndi akuluakulu ena amene anabwerawo kuti, “Kodi
Ine ndikutsogolera gulu lowukira kuti mubwere ndi malupanga ndi
zibonga? 53 Tsiku lililonse ndinali nanu m’mabwalo a m’Nyumba ya
Mulungu ndipo inu simunandigwire. Koma iyi ndi nthawi yanu pamene
mdima ukulamulira.”

### *Petro Akana Yesu*

54 Pamenepo anamugwira Iye, napita naye ndipo anamutengera ku
nyumba ya mkulu wa ansembe. Petro anamutsatira patali. 55 Koma
pamene anasonkha moto pakati pa bwalo la milandu, anakhala onse pansi
ndipo Petro anakhalanso pansi. 56 Mtsikana wantchito anamuona atakhala
nawo pafupi ndi moto. Iye anamuyang’anitsitsa ndipo anati, “Munthu uyu
anali ndi Yesu.”

57 Koma Petro anakana nati, “Mtsikana, ine sindimudziwa ameneyu.”

58 Patatha kanthawi pang’ono, wina wake anamuona ndipo anati,
“Iwenso ndiwe mmodzi mwa iwo.”

Petro anayankha kuti, “Munthu iwe, ayi sindine.”

59 Patatha pafupifupi ora limodzi, munthu winanso anati, “Zoonadi,
munthu uyu anali ndi Iye, pakuti ndi mu Galileya.”

60 Petro anayankha kuti, “Munthu iwe, sindikudziwa zimene ukunena
apa.” Pamene iye ankayankhula, tambala analira. 61 Ambuye anachewuka
namuyang’anitsitsa Petro. Pamenepo Petro anakumbukira mawu amene
Ambuye anayankhula kwa iye kuti, “Asanalire tambala lero lino,
udzandikana Ine katatu.” 62 Ndipo iye anapita panja nakalira kwambiri.

### *Asilikali Amuchita Chipongwe Yesu*

63 Anthu amene ankalonda Yesu anayamba kumuchita chipongwe ndi
kumumenya. 64 Anamumanga m'maso ndi kumufunsa kuti, "Tanenera!
Wakumenya iwe ndi ndani?" 65 Ndipo iwo anamunena zachipongwe
zambiri.

### *Yesu Pamaso pa Pilato ndi Herode*

66 Kutacha, bungwe la akuluakulu, pamodzi ndi akulu a ansembe
ndi aphunzitsi amalamulo, anakumana pamodzi, ndipo anamuyika Yesu
patsogolo pawo. 67 Iwo anati, "Tiwuze, ngati ndiwe Khristu."

Yesu anayankha kuti, "Ine nditakuwuzani simungandikhulupirire.
68 Ine nditakufunsani inu, simungandiyankhe. 69 Koma kuyambira
tsopano, Mwana wa Munthu adzakhala ku dzanja lamanja la Mulungu
wamphamvu."

70 Onse anafunsa kuti, "Ndiye kuti ndiwe Mwana wa Mulungu?"

Iye anayankha kuti, "Mwanena ndinu kuti Ndine."

71 Pamenepo iwo anati, "Nanga tikufuniranjinso umboni wina? Ife
tamva kuchokera pa milomo yake."

# 23

1 Kenaka gulu lonse la anthuwo linayimirira ndi kumutengera kwa
Pilato. 2 Ndipo iwo anayamba kumuneneza nati, "Ife tinapeza munthu uyu
akusokoneza anthu a mtundu wathu ndipo amatsutsa zopereka msonkho
kwa Kaisara komanso amati ndi Khristu, Mfumu."

3 Pamenepo Pilato anamufunsa Yesu kuti, "Kodi Iwe ndiwe Mfumu ya
Ayuda?"

Yesu anayankha kuti, "Mwatero ndinu."

4 Kenaka Pilato anawawuza akulu a ansembe ndi gulu la anthu, "Ine
sindikumupeza cholakwa munthuyu."

5 Koma iwo analimbikirabe kuti, "Iyeyu amasokoneza anthu ku Yudeya
konse ndi chiphunzitso chake, Iyeyu anayambira ku Galileya ndipo
wayenda mtunda wonse mpaka kuno."

6 Pakumva zimenezi, Pilato anafunsa ngati munthuyo ndi Mgalileya.
7 Iye atamva kuti Yesu anali pansi pa ulamuliro wa Herode, anamutumiza
kwa Herodeyo, amene pa nthawi imeneyo analinso mu Yerusalemu.

8 Herode ataona Yesu, anakondwa kwambiri, chifukwa kwa nthawi
yayitali, ankafunitsitsa atamuona. Kuchokera pa zimene anamva za
Iye, anayembekezera kuti achita zodabwitsa. 9 Iye anamufunsa mafunso
ambiri, koma Yesu sanayankhe. 10 Akulu a ansembe ndi aphunzitsi amala-
mulo, anayimirira pamenepo ndi kumuneneza kwambiri. 11 Pamenepo
Herode ndi asilikali ake anamuseka ndi kumunyoza Iye. Atamuveka
mkanjo wonyezimira, anamutumizanso kwa Pilato. 12 Tsiku limenelo,
Herode ndi Pilato anakhala abwenzi. Zisanachitike izi anali adani.

13 Pilato anasonkhanitsa akulu a ansembe, oweruza ndi anthu,
14 ndipo anawawuza kuti, "Munabweretsa munthuyu kwa ine ngati ndiye
amawuza anthu kuti awukire. Ine ndamufunsa pamaso panu ndipo
sindinapeze chomuyimbira mlandu. 15 Herodenso sanapeze chifukwa
pakuti wamutumizanso kwa ife monga mmene mukuoneramu. Iyeyu
sanachite chinthu chakuti aphedwe. 16 N'chifukwa chake, ine ndingo-
mulanga, n'kumumasula." 17 (Pa nthawi yachikondwerero cha Paska iye
ankayenera kumasula munthu mmodzi).

18 Onse pamodzi anafuwula kuti, "Muchotseni munthuyu! Timasulireni
Baraba!" 19 (Baraba anaponyedwa m'ndende chifukwa choyambitsa
chipolowe mu mzinda ndi kupha).
20 Pofuna kumumasula Yesu, Pilato anawadandaulira iwo. 21 Koma iwo
anapitirirabe kufuwula kuti, "Mpachikeni! Mpachikeni!"
22 Kachitatu anawafunsanso iwo kuti, "Chifukwa chiyani? Kodi munthu
uyu wachita choyipa chanji? Ine sindinapeze cholakwa mwa Iye chakuti
aphedwe choncho ndingomukwapula ndi kumumasula."
23 Koma ndi mawu ofuwulitsa, analimbikirabe kuti Iye apachikidwe,
ndipo kufuwulako kunapitirira. 24 Choncho Pilato anatsimikiza kuchita
zofuna zawozo. 25 Iye anawamasulira munthu amene anaponyedwa
m'ndende chifukwa choyambitsa chipolowe ndi kupha, amene ankamu-
funayo, ndipo anawapatsa Yesu mwakufuna kwawo.

*Kupachikidwa kwa Yesu*

26 Ndipo pamene ankapita naye, anagwira Simoni wa ku Kurene,
amene ankachokera ku munda, namusenzetsa mtanda namuyendetsa
pambuyo pa Yesu. 27 Gulu lalikulu la anthu linamutsata Iye, kuphatikiza
amayi amene ankabuma ndi kumulirira. 28 Yesu anatembenuka nati
kwa iwo, "Ana aakazi a Yerusalemu, musandilirire Ine; dzilirireni nokha
ndi ana anu. 29 Pakuti nthawi idzabwera imene inu mudzati, 'Ndi
odala amayi osabereka, mimba zimene sizinabereke ndi mawere amene
sanayamwitse!' 30 Kenaka,
"adzawuza mapiri kuti tigwereni ife;
zitunda kuti tiphimbeni ife.
31 Chifukwa ngati anthu akuchita izi pa mtengo wauwisi, chidzachitike
n'chiyani ndi wowuma?"
32 Amuna ena awiri, onsewo achifwamba, anatengedwanso pamodzi
ndi Yesu kukaphedwa. 33 Pamene anafika pamalo otchedwa Bade,
anamupachika Iye pamodzi ndi achifwambawo, mmodzi kudzanja lake
lamanja ndi winayo la ku lamazere. 34 Yesu anati, "Atate, akhululukireni,
pakuti sakudziwa chimene akuchita." Ndipo anagawana malaya ake
mochita maere.
35 Anthu anayimirira n'kumaonerera, ngakhalenso akuluakulu ankamu-
lalatira Iye. Iwo anati, "Iye anapulumutsa ena; adzipulumutse yekha ngati
ndi Khristu wa Mulungu, Wosankhidwayo."
36 Asilikalinso anabwera ndi kumunyoza Iye. Iwo anamupatsa vinyo
wosasa, 37 ndipo anati, "Ngati ndiwe Mfumu ya Ayuda, dzipulumutse
wekha."
38 Ndipo panalembedwa chikwangwani pamwamba pake chimene
chinati: UYU NDI MFUMU YA AYUDA.
39 Mmodzi wa achifwambawo, amene anapachikidwa, anamunenera Iye
zamwano nati, "Kodi sindiwe Khristu? Dzipulumutse wekha ndi ifenso!"
40 Koma wachifwamba winayo anamudzudzula iye nati, "Suopa Mu-
lungu, iwenso ukulandira chilango chomwechi? 41 Ife tikulangidwa
mwachilungamo, pakuti ife tikulandira monga mwa ntchito zathu. Koma
munthu uyu sanachimwe kanthu."
42 Kenaka anati, "Yesu, mundikumbukire ine pamene mulowa mu
ufumu wanu."
43 Yesu anayankha kuti, "Zoonadi, ndikukuwuza kuti lero lino udzakhala
ndi Ine m'paradaiso."

### *Imfa ya Yesu*

44 Linali tsopano pafupi ora lachisanu ndi chimodzi, ndipo mdima
unagwa pa dziko lonse mpaka ora lachisanu ndi chinayi, 45 pakuti
dzuwa linaleka kuwala. Ndipo chinsalu cha m'Nyumba ya Mulungu
chinang'ambika pakati. 46 Yesu anafuwula ndi mawu okweza kuti,
"Atate, ndikupereka mzimu wanga m'manja mwanu." Atanena zimenezi,
anamwalira.
47 Kenturiyo, ataona zimene zinachitikazi, analemekeza Mulungu ndipo
anati, "Zoonadi, uyu anali munthu wolungama." 48 Anthu onse amene
anasonkhana kudzaonerera izi, ataona zinachitikazo, anadziguguda
pachifuwa ndipo anachoka. 49 Koma onse amene anamudziwa Iye,
kuphatikiza amayi amene anamutsatira kuchokera ku Galileya, anay-
imirira akuona zinthu izi.

### *Yesu Ayikidwa M'manda*

50 Ndipo taonani panali munthu wina wotchedwa Yosefe, mmodzi wa
gulu loweruza, munthu wabwino ndi wolungama. 51 Iye sanavomereze
zimene anzake abwalo anagwirizana ndi kuchita. Iye ankachokera ku
mudzi wa Arimateyu wa ku Yudeya ndipo ankayembekezera ufumu wa
Mulungu. 52 Atapita kwa Pilato, iye anakapempha mtembo wa Yesu.
53 Ndipo anawutsitsa, nawukulunga nsalu yabafuta nawuyika m'manda
wosemedwa m'mwala, amene panalibe wina amene anayikidwamo.
54 Linali tsiku lokonzekera ndipo Sabata linatsala pang'ono kuyamba.
55 Amayi amene anabwera ndi Yesu kuchokera ku Galileya, anatsata
Yosefe ndipo anaona manda ndi momwe mtembo wake anawuyikira.
56 Kenaka anapita ku mudzi ndi kukakonza mafuta onunkhira. Koma
anapuma pa tsiku la Sabata pomvera malamulo.

## 24

### *Yesu Auka kwa Akufa*

1 Pa tsiku loyamba la Sabata, mmamawa kwambiri, amayi anatenga zo-
nunkhira napita ku manda. 2 Anaona mwala wa pa manda utagubuduzika
3 ndipo atalowamo sanapeze mtembo wa Ambuye Yesu. 4 Pamene
iwo ankadabwa za zimenezi, mwadzidzidzi, amuna awiri ovala zovala
zonyezimira kwambiri anayimirira pambali pawo. 5 Ndi mantha, amayiwo
anaweramitsa nkhope zawo pansi, koma amunawo anawawuza kuti,
"N'chifukwa chiyani mukufuna wamoyo pakati pa akufa? 6 Iye sali muno
ayi. Wauka! Kumbukirani zimene anakuwuzani pamene anali nanu
ku Galileya: 7 'Mwana wa Munthu ayenera kuperekedwa m'manja mwa
anthu ochimwa, napachikidwa ndipo tsiku lachitatu adzaukitsidwanso.' "
8 Ndipo anakumbukira mawu ake.
9 Atabwerera kuchokera ku mandako, anafotokoza zinthu zonse kwa
khumi ndi mmodziwo ndi kwa ena onse. 10 Amayi anali Mariya
Magadalena, Yohana, Mariya amayi a Yakobo, ndi ena anali nawo amene
anawuza atumwi. 11 Koma iwo sanawakhulupirire amayiwa, chifukwa
mawu awo amaoneka kwa iwo ngati opanda nzeru. 12 Komabe Petro
anayimirira ndi kuthamangira ku manda. Atasuzumira, anaona nsalu
zimene anamukulungira zija zili pa zokha, ndipo iye anachoka, akudabwa
ndi zimene zinachitikazo.

### *Zochitika pa Njira ya ku Emau*

13 Ndipo tsiku lomwelo, awiri a iwo ankapita ku mudzi wotchedwa
Emau, pafupifupi makilomita khumi ndi imodzi kuchokera ku
Yerusalemu. 14 Iwo ankayankhulana za zonse zimene zinachitikazo.
15 Pamenepo Yesu mwini wake anabwera ndi kuyenda nawo pamodzi;
16 koma iwo sanamuzindikire.
17 Iye anawafunsa kuti, "Kodi mukukambirana zotani m'njira muno?"

Iwo anayima ndi nkhope zakugwa. 18 Mmodzi wa iwo wotchedwa
Kaliyopa anamufunsa kuti, "Kodi ndiwe wekha wokhala mu Yerusalemu
amene sukudziwa zinthu zimene zachitika m'masiku awa?"
19 Iye anafunsa kuti, "Zinthu zotani?"

Iwo anayankha nati, "Za Yesu wa ku Nazareti, Iye anali mneneri,
wamphamvu m'mawu ndi mu zochita pamaso pa Mulungu ndi anthu
onse. 20 Akulu a ansembe ndi oweruza anamupereka Iye kuti aphedwe,
ndipo anamupachika Iye; 21 koma ife tinkayembekezera kuti Iye ndiye
amene akanawombola Israeli. Ndipo kuwonjeza apo, lero ndi tsiku
lachitatu chichitikireni izi. 22 Kuwonjezanso apo, ena mwa amayi athu
atidabwitsa ife. Iwo anapita ku manda mmamawa 23 koma sanakapeze
mtembo wake. Iwo anabwera ndi kudzatiwuza ife kuti anaona masom-
phenya a angelo amene anati Yesu ali moyo. 24 Kenaka ena mwa anzathu
anapita ku manda ndipo anakapeza monga momwe amayiwo ananenera,
koma Iye sanamuone."

25 Iye anawawuza kuti, "Inu ndinu anthu opusa, osafuna kukhulupirira
msanga zonse zimene aneneri ananena! 26 Kodi Khristu sanayenera
kumva zowawa izi ndipo kenaka ndi kulowa mu ulemerero wake?"
27 Ndipo kuyambira ndi Mose ndi aneneri onse Iye anawafotokozera
zimene zinalembedwa m'malemba wonse zokhudzana ndi Iye mwini.

28 Atayandikira mudzi omwe amapitako, Yesu anachita ngati akupitirira.
29 Koma iwo anamupempha Iye kwambiri kuti, "Mukhale ndi ife, popeza
kwatsala pang'ono kuda, ndipo dzuwa lili pafupi kulowa." Ndipo Iye
anapita kukakhala nawo.

30 Iye ali pa tebulo pamodzi nawo, anatenga buledi ndipo anayamika,
nanyema nayamba kuwagawira. 31 Kenaka maso awo anatsekuka ndipo
anamuzindikira Iye, ndipo anachoka pakati pawo. 32 Iwo anafunsana
wina ndi mnzake kuti, "Kodi mitima yathu sinali kutentha m'kati mwathu
pamene Iye ankayankhulana nafe pa njira ndi mmene anatitsekulira
malemba?"
33 Nthawi yomweyo iwo anayimirira ndi kubwerera ku Yerusalemu.
Iwo anapeza khumi ndi mmodziwo ndi ena anali nawo nasonkhana
pamodzi 34 ndipo anati, "Ndi zoonadi! Ambuye auka ndipo anaonekera
kwa Simoni." 35 Kenaka awiriwo anawawuza zimene zinachitika pa njira,
ndi mmene iwo anamudziwira Yesu, Iye atanyema buledi.

### *Yesu Aonekera kwa Ophunzira*

36 Akufotokoza zimenezi, Yesu mwini wake anayimirira pakati pawo
ndipo anati, "Mukhale ndi mtendere."

37 Koma chifukwa choti anathedwa nzeru ndi kuchita mantha, ank-
aganiza kuti akuona mzukwa. 38 Iye anawafunsa kuti, "N'chifukwa
chiyani mukuvutika? N'chifukwa chiyani mukukayika mu mtima mwanu?
39 Taonani manja anga ndi mapazi anga. Ine ndine amene! Khudzeni kuti
muone. Mzukwa ulibe mnofu ndi mafupa monga mukuonera ndili nazo."

40 Iye atanena izi anawaonetsa manja ake ndi mapazi ake. 41 Ndipo
pamene iwo samakhulupirirabe, chifukwa cha chimwemwe ndi kudabwa,
Iye anawafunsa kuti, "Kodi muli ndi chakudya chilichonse pano?" 42 Iwo
anamupatsa Iye kachidutswa ka nsomba yophika. 43 Iye anakatenga ndi
kukadya iwo akuona.

44 Iye anawawuza kuti, "Izi ndi zimene ndinakuwuzani pamene ndinali
nanu: chilichonse chiyenera kukwaniritsidwa chimene chinalembedwa
cha Ine m'buku la Malamulo a Mose, Aneneri ndi Masalimo."

45 Kenaka anawatsekula maganizo kuti azindikire Malemba. 46 Iye
anawawuza kuti, "Izi ndi zimene zinalembedwa: Khristu adzazunzika
ndipo adzauka kwa akufa tsiku lachitatu. 47 Ndipo kutembenuka mtima
ndi kukhululukidwa kwa machimo zidzalalikidwa mu dzina lake kwa
anthu amitundu yonse kuyambira mu Yerusalemu. 48 Inu ndinu mboni
za zimenezi. 49 Ine ndidzakutumizirani chimene Atate anga analonjeza.
Koma khalani mu mzinda muno mpaka mutavekedwa mphamvu yochok-
era kumwamba."

### *Kupita Kumwamba*

50 Iye atawatengera kunja kwa mzindawo mpaka ku Betaniya, anakweza
manja ake ndi kuwadalitsa. 51 Iye akuwadalitsa, anawasiya ndipo
anatengedwa kupita kumwamba. 52 Pamenepo anamulambira Iye ndipo
anabwerera ku Yerusalemu ndi chimwemwe chachikulu. 53 Ndipo iwo
anakhalabe ku Nyumba ya Mulungu, akulemekeza Mulungu.

# UTHENGA WABWINO WA YESU KHRISTU WOLEMBEDWA NDI YOHANE

### *Mawu Asandulika Thupi*

1 Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali kwa Mulungu, ndipo
Mawu ndiye Mulungu. 2 Mawuwa anali ndi Mulungu pachiyambi.
3 Zinthu zonse zinalengedwa ndi Iye; ndipo popanda Iye sikukanakhala
kanthu kalikonse kolengedwa. 4 Mwa Iye munali moyo, ndipo moyowo
unali kuwunika kwa anthu. 5 Kuwunika kunawala mu mdima, koma
mdimawo sunakuzindikire.
6 Kunabwera munthu amene anatumizidwa kuchokera kwa Mulungu;
Iyeyo dzina lake linali Yohane. 7 Iye anabwera ngati mboni kudzachitira
umboni kuwunikako kuti kudzera mwa iye anthu onse akhulupirire.
8 Iyeyu sanali kuwunika; koma anabwera ngati mboni ya kuwunika.
9 Kuwunika koona kumene kuwunikira munthu aliyense kunabwera ku
dziko lapansi.
10 Iye anali m'dziko lapansi, ndipo ngakhale kuti dziko lapansi
linalengedwa ndi Iye, dziko lapansilo silinamuzindikire Iye. 11 Iye
anabwera kwa iwo amene anali akeake, koma akewo sanamulandire Iye.
12 Koma kwa onse amene anamulandira Iye, kwa amene anakhulupirira
m'dzina lake, Iye anawapatsa mphamvu yokhala ana a Mulungu; 13 ana
wobadwa osati monga mwachilengedwe, kapena chisankho cha munthu,
kapena chifuniro cha mwamuna koma wobadwa mwa Mulungu.
14 Mawu anasandulika thupi ndipo anakhala pakati pathu. Ife tinaona
ulemerero wake, ulemerero wa Iye amene ndi Mwana mmodzi yekhayo
wa Atate, wodzaza ndi chisomo ndi choonadi.
15 Yohane achitira umboni za Iye. Iye akufuwula kuti, "Uyu ndi Iye
amene ndinati, 'Iye amene akubwera pambuyo panga ndi wondiposa ine
chifukwa, Iyeyo analipo ine ndisanabadwe.' " 16 Kuchokera m'kuchuluka
kwa chisomo chake ife tonse talandira madalitso pamwamba pa madalitso.
17 Pakuti lamulo linapatsidwa kudzera mwa Mose; chisomo ndi choonadi
zinabwera kudzera mwa Yesu Khristu. 18 Palibe munthu amene anaona
Mulungu, koma Mwana mmodzi yekhayo amene ali wa pamtima pa Atate,
ndiye anafotokoza za Iye.

### *Yohane M'batizi Akana kuti Iye ndi Khristu*

19 Tsopano uwu ndi umboni wa Yohane pamene Ayuda a ku Yerusalemu
anatumiza ansembe ndi Alevi kudzamufunsa kuti iye anali yani. 20 Iye
sanalephere kuvomereza, koma iye anavomereza momasuka kuti, "Ine
sindine Khristu."
21 Iwo anamufunsa kuti, "Nanga iwe ndiwe yani? Kodi ndiwe Eliya?"
Iye anati, "Sindine."
"Kodi ndiwe Mneneri?"
Iye anayankha kuti, "Ayi."
22 Pomaliza iwo anati, "Ndiwe yani? Tipatse yankho kuti tipite nalo kwa
amene anatituma. Kodi iwe ukuti chiyani za iwe mwini?"
23 Yohane anayankha ndi mawu a mneneri Yesaya kuti, "Ine ndi mawu
a wofuwula m'chipululu, 'Wongolani njira ya Ambuye.' "

24 Tsopano Afarisi ena amene anatumidwa 25 anamufunsa Iye kuti,
“Kodi ndi chifukwa chiyani, umabatiza ngati iwe si Khristu, kapena Eliya,
kapena Mneneri?”
26 Yohane anayankha kuti, “Ine ndimabatiza ndi madzi, koma pakati
panu payima amene simukumudziwa. 27 Iye ndi amene akubwera
pambuyo panga, ine siwoyenera kumasula zingwe za nsapato zake.”
28 Zonsezi zinachitika ku Betaniya kutsidya lina la mtsinje wa Yorodani,
kumene Yohane ankabatizira.

### *Yesu Mwana Wankhosa wa Mulungu*

29 Pa tsiku lotsatira Yohane anaona Yesu akubwera kwa iye ndipo anati,
“Taonani, Mwana Wankhosa wa Mulungu, amene achotsa tchimo la dziko
lapansi! 30 Uyu ndi amene ndimatanthauza pamene ndinanena kuti,
‘Munthu amene akubwera pambuyo panga ndi wondiposa ine chifukwa
analipo ine ndisanabadwe.’ 31 Ine mwini sindinamudziwe Iye, koma
ndinabwera kubatiza ndi madzi kuti Iye adziwike mu Israeli.”
32 Kenaka Yohane anapereka umboni uwu: “Ine ndinaona Mzimu
Woyera ngati nkhunda kuchokera kumwamba nakhala pa Iye. 33 Ine
sindikanamudziwa Iye, koma kuti amene ananditumа ine kudzabatiza ndi
madzi anati kwa ine, ‘Munthu amene udzaona Mzimu Woyera akutsika
nakhazikika pa Iye ndi amene adzabatize ndi Mzimu Woyera.’ 34 Ine
ndaona ndipo ndikuchitira umboni kuti uyu ndi Mwana wa Mulungu.”

### *Ophunzira Oyamba a Yesu*

35 Pa tsiku lotsatira Yohane analinso pamenepo pamodzi ndi awiri a
ophunzira ake. 36 Iye ataona Yesu akudutsa anati, “Taonani Mwana
Wankhosa wa Mulungu!”
37 Ophunzira ake awiriwo atamva iye akunena izi, iwo anamutsatira
Yesu. 38 Atatembenuka, Yesu anaona iwo akumutsatira ndipo anawafunsa
kuti, “Kodi mukufuna chiyani?”
Iwo anati, “Rabi (kutanthauza kuti Aphunzitsi), kodi mukukhala kuti?”
39 Iye anayankha kuti, “Bwerani mudzaone.”
Choncho iwo anapita ndi kukaona kumene Iye amakhala, ndipo
anakhala naye tsiku limenelo. Linali ngati pafupifupi ora la khumi.
40 Andreya m’bale wake wa Simoni Petro, anali mmodzi wa awiriwo
amene anamva zimene Yohane ananena ndiponso amene anamutsata
Yesu. 41 Choncho chimene Andreya anachita ndi kukapeza m’bale wake
Simoni ndipo anamuwuza kuti, “Ife tamupeza Mesiya,” (kutanthauza kuti
Khristu).
42 Kenaka iye anabweretsa Simoni kwa Yesu, amene anamuyang’ana
ndipo anati, “Iwe ndiwe Simoni, mwana wa Yohane. Udzatchedwa Kefa”
(limene litanthauza kuti Petro).

### *Yesu Ayitana Filipo ndi Natanieli*

43 Pa tsiku lotsatira Yesu anaganiza zopita ku Galileya. Atamupeza Filipo,
anati kwa iye, “Nditsate.”
44 Filipo monga Andreya ndi Petro, anali wochokera ku mzinda mudzi
Betisaida. 45 Filipo anakapeza Natanieli ndipo anamuwuza kuti, “Ife
tapeza amene Mose analemba za Iye m’malamulo, ndi zimene aneneri
analembanso za Iye, Yesu wa ku Nazareti, mwana wa Yosefe.”
46 Natanieli anafunsa kuti, “Nazareti! Kodi kanthu kalikonse kabwino
kangachokere kumeneko?”

Filipo anati, “Bwera udzaone.”
47 Yesu atamuona Natanieli akuyandikira, anati kwa iye, “Uyu ndi
Mwisraeli weniweni, mwa iye mulibe chinyengo.”
48 Natanieli anafunsa kuti, “Kodi mwandidziwa bwanji?”
Yesu anayankha kuti, “Ine ndinakuona iwe utakhala pansi pamtengo
wamkuyu Filipo asanakuyitane.”
49 Kenaka Natanieli ananena kuti, “Rabi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu;
Inu ndinu Mfumu ya Israeli.”
50 Yesu anati, “Ukukhulupirira chifukwa chakuti ndakuwuza kuti Ine
ndinakuona iwe uli pansi pamtengo wamkuyu? Iwe udzaona zinthu
zazikulu kuposa izo.” 51 Ndipo Iye anapitirira kuti, “Zoonadi, Ine
ndikuwuza kuti iwe udzaona kumwamba, kutatsekuka ndi angelo a
Mulungu akukwera ndi kutsika pa Mwana wa Munthu.”

# 2

### *Yesu Asandutsa Madzi Kukhala Vinyo*

1 Pa tsiku lachitatu munali ukwati mu Kana wa ku Galileya. Amayi ake
a Yesu anali komweko, 2 ndipo Yesu ndi ophunzira ake anayitanidwanso
ku ukwatiwo. 3 Vinyo atatha, amayi a Yesu anati kwa Iye, “Wawathera
vinyo.”
4 Yesu anayankha kuti, “Amayi, chifukwa chiyani mukundiwuza Ine?
Nthawi yanga sinakwane.”
5 Amayi ake anati kwa antchito, “Inu muchite chilichonse chimene
akuwuzeni.”
6 Pamenepo panali mitsuko yamiyala yothiramo madzi isanu ndi
umodzi, imene Ayuda amagwiritsa ntchito pa mwambo wodziyeretsa.
Uliwonse unali ndi malita 100 kapena kupitirirapo.
7 Yesu anati kwa antchitowo, “Dzazani madzi m’mitsukoyi,” ndipo iwo
anadzaza ndendende.
8 Ndipo Iye anatinso kwa iwo, “Tsopano tungani ndipo kaperekeni kwa
mkulu waphwando.”
Iwo anachita momwemo. 9 Mkulu waphwando analawa madziwo
amene anasandulika vinyo, ndipo sanazindikire kumene vinyoyo ana-
chokera, ngakhale kuti antchito amene anatunga madziwo amadziwa.
Kenaka anayitanira mkwati pambali 10 ndipo anati, “Aliyense amatulutsa
vinyo wokoma kwambiri poyambirira ndipo kenaka vinyo wosakoma
pamene oyitanidwa atamwa kale wambiri; koma iwe wasunga wokoma
mpaka tsopano.”
11 Ichi chinali chizindikiro chodabwitsa choyamba chimene Yesu ana-
chita ku Kana wa ku Galileya. Potero Iye anawulula ulemerero wake,
ndipo ophunzira ake anamukhulupirira Iye.

### *Yesu Ayeretsa Nyumba ya Mulungu*

12 Zitatha izi Iye anatsikira ku Kaperenawo pamodzi ndi amayi ake, abale
ake ndi ophunzira ake. Iwo anakhala kumeneko masiku owerengeka.
13 Nthawi ya Paska ya Ayuda itayandikira, Yesu anapita ku Yerusalemu.
14 M’bwalo la Nyumba ya Mulungu Iye anapeza anthu akugulitsa
ng’ombe, nkhosa ndi nkhunda ndipo ena akusintha ndalama pa matebulo.
15 Chifukwa cha zimenezi Iye anapanga chikwapu cha zingwe ndipo
anatulutsa onse m’bwalo la Nyumbayo, pamodzi ndi nkhosa ndi ng’ombe;
Iye anamwaza ndalama zawo ndi kugudubuza matebulo. 16 Kwa amene

amagulitsa nkhunda, Iye anati, "Tulutsani izi muno! Osasandutsa Nyumba ya Atate anga msika!"
17 Ophunzira ake anakumbukira kuti zinalembedwa kuti, "Kudzipereka kwanga ku nyumba yanu kudzandiphetsa."
18 Kenaka Ayuda anamufunsa Yesu kuti, "Kodi mungationetse chizindikiro chodabwitsa chotani chotsimikizira ulamuliro wanu wochitira izi?"
19 Yesu anawayankha kuti, "Gwetsani Nyumba ya Mulunguyi ndipo Ine ndidzayimanganso m'masiku atatu."
20 Ayuda anayankha kuti, "Zinatenga zaka makumi anayi kumanga Nyumbayi, kodi Inu mungayimange masiku atatu?" 21 Koma Nyumba ya
Mulungu imene amanena linali thupi lake. 22 Iye ataukitsidwa kwa akufa, ophunzira ake anakumbukira zimene Iye ananena ndipo anakhulupirira Malemba ndi mawu amene Yesu anayankhula.
23 Tsopano Iye ali mu Yerusalemu pa phwando la Paska, anthu ambiri anaona zizindikiro zodabwitsa zimene amachita ndipo anakhulupirira
dzina lake. 24 Koma Yesu sanawakhulupirire iwo, pakuti amadziwa anthu
onse. 25 Iye sanafune umboni wa wina aliyense popeza amadziwa zomwe zinali m'mitima mwa anthu.

# 3

*Yesu Aphunzitsa Nekodimo za Kubadwa Kwatsopano*

1 Ndipo panali Mfarisi wotchedwa Nekodimo, wa m'gulu lolamulira la
Ayuda. 2 Iye anabwera kwa Yesu usiku ndipo anati, "Rabi, ife tikudziwa kuti ndinu aphunzitsi wochokera kwa Mulungu, pakuti palibe amene angachite zizindikiro zodabwitsa zimene Inu mukuchita ngati Mulungu sali naye."
3 Poyankha Yesu ananena kuti, "Zoonadi, Ine ndikukuwuza kuti, ngati munthu sabadwanso mwatsopano sangathe kuona ufumu wa Mulungu."
4 Nekodimo anati, "Kodi munthu angabadwenso bwanji atakalamba? Kodi angalowe kachiwiri m'mimba ya amayi ake kuti abadwenso?"
5 Yesu anayankha kuti, "Zoonadi, Ine ndikukuwuza kuti ngati munthu sabadwa mwa madzi ndi Mzimu Woyera, sangalowe mu ufumu wa Mu-
lungu. 6 Thupi limabereka thupi, koma Mzimu amabereka mzimu. 7 Iwe
usadabwe chifukwa ndakuwuza kuti, 'Uyenera kubadwanso.' 8 Mphepo imawomba kulikonse kumene ikufuna. Ungathe kumva kuwomba kwake, koma sungathe kudziwa kumene ikuchokera kapena kumene ikupita. N'chimodzimodzi ndi amene abadwa ndi Mzimu Woyera."
9 Nekodimo anafunsa kuti, "Kodi izi zingatheke bwanji?"
10 Yesu anati, "Iwe mphunzitsi wa Israeli, kodi sukuzindikira zimenezi?
11 Zoonadi, Ine ndikukuwuza kuti ife tiyankhula zimene tikuzidziwa ndi kuchitira umboni zimene taziona, komabe inu simuvomereza umboni
wathu. 12 Ine ndikuyankhula kwa iwe zinthu za dziko lapansi ndipo sukukhulupirira. Nanga kodi udzakhulupirira bwanji ngati nditayankhula
zinthu zakumwamba? 13 Palibe wina aliyense anapita kumwamba, koma yekhayo amene watsika kuchokera kumwamba, Mwana wa Munthu.
14 Tsono monga Mose anapachika njoka m'chipululu, moteronso Mwana
wa Munthu ayenera kupachikidwa, 15 kuti aliyense amene akhulupirira Iye akhale ndi moyo wosatha.
16 "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi, kotero anapereka Mwana wake wobadwa yekha, kuti aliyense wokhulupirira Iye asatayike koma

akhale ndi moyo wosatha. 17 Pakuti Mulungu sanatume Mwana wake
ku dziko lapansi, kuti akaweruze, koma kuti akapulumutse dziko
lapansi. 18 Aliyense wokhulupirira Iye saweruzidwa, koma aliyense
wosakhulupirira waweruzidwa kale chifukwa sanakhulupirire dzina la
Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. 19 Ndipo chiweruzo ndi ichi: kuwu-
nika kunabwera m'dziko lapansi, koma anthu anakonda mdima m'malo
mwa kuwunikako, chifukwa ntchito zawo zinali zoyipa. 20 Aliyense
wochita zoyipa amadana ndi kuwunika, ndipo sabwera poyera chifukwa
cha mantha kuti ntchito zake zingaonekere. 21 Koma aliyense wokhala
mu choonadi amabwera ku kuwunika, kuti zionekere poyera zimene iye
wachita zachitika kudzera mwa Mulungu."

### *Yohane M'batizi Achita Umboni za Yesu*

22 Zitatha izi, Yesu ndi ophunzira ake anapita m'madera a ku midzi ya ku
Yudeya, kumene Iye anakhala kanthawi akubatiza. 23 Ndipo Yohane ama-
batizanso ku Ainoni kufupi ndi Salimu, chifukwa kumeneko kunali madzi
ambiri ndipo anthu amabwererabwererabe kudzabatizidwa. 24 (Apa
n'kuti Yohane asanatsekeredwe m'ndende). 25 Mkangano unabuka pakati
pa ophunzira ena a Yohane ndi Ayuda ena pa zamwambo wodziyeretsa wa
Ayuda. 26 Iwo anabwera kwa Yohane anati, "Rabi, munthu uja munali naye
mbali inayo ya mu mtsinje wa Yorodani, amene munamuchitira umboni,
taonani naye akubatizanso, ndipo aliyense akupita kwa Iye."

27 Atamva zimenezi, Yohane anayankha kuti, "Munthu amalandira
chokhacho chapatsidwa kwa iye kuchokera kumwamba. 28 Inuyo ndinu
mboni zanga kuti ine ndinati, 'Ine sindine Khristu koma ndatumidwa
patsogolo pa Iye.' 29 Mwini wake wa mkwatibwi ndi mkwati. Ndipo
bwenzi lamkwati limadikira ndi kumvetsera iye, ndipo amakondwa
akamva mawu a mkwatiyo. Ine changa ndi chimwemwe ndipo ndine
wosangalala kwambiri. 30 N'koyenera kuti Iyeyo akule, ine ndichepe.

31 "Iye wochokera kumwamba ndi wapamwamba pa onse: iye wo-
chokera m'dziko lapansi ndi wa dziko lapansi, ndipo amayankhula
monga mmodzi wa adziko lapansi. Iye wochokera kumwamba ndi
wopambana onse. 32 Iye achita umboni pa zimene waziona ndi kuzimva,
koma palibe avomereza umboni wake. 33 Munthu amene amawulandira
akutsimikizira kuti Mulungu ndi woona. 34 Pakuti amene Mulungu
wamutuma amayankhula mawu a Mulungu; Mulungu wamupatsa Mzimu
Woyera mopanda malire. 35 Atate amakonda Mwana ndipo apereka
zonse m'manja mwake. 36 Aliyense wokhulupirira Mwanayo ali ndi moyo
wosatha, koma iye amene samvera Mwanayo sadzawuona moyo, pakuti
mkwiyo wa Mulungu umakhala pa iye."

## 4

### *Yesu Acheza ndi Mayi wa ku Samariya*

1 Yesu atazindikira kuti Afarisi amva zoti Iye ankapeza ndi kubatiza
ophunzira ambiri kupambana Yohane, 2 (ngakhale kuti Yesuyo sankaba-
tiza, koma ophunzira ake). 3 Iye anachoka ku Yudeya ndi kubwereranso
ku Galileya.

4 Ndipo Iye anayenera kudutsa mu Samariya. 5 Iye anafika m'mudzi wa
Asamariya wotchedwa Sukari, pafupi ndi malo amene Yakobo anapatsa
mwana wake Yosefe. 6 Chitsime cha Yakobo chinali pamenepo ndipo Yesu

atatopa ndi ulendo anakhala pansi pambali pa chitsimecho. Nthawi inali
pafupifupi ora lachisanu ndi chimodzi masana.
7 Mayi wa Chisamariya atabwera kudzatunga madzi, Yesu anati kwa
iye, “Kodi ungandipatse madzi akumwa.” 8 (Ophunzira ake n’kuti atapita
m’mudzi kukagula chakudya).
9 Mayiyo anati kwa Iye, “Inu ndinu Myuda ndipo ine ndine Msamariya.
Bwanji mukundipempha madzi akumwa?” (Popeza Ayuda ndi Asamariya
sankayanjana).
10 Yesu anamuyankha kuti, “Koma iwe ukanadziwa mphatso ya Mulungu
ndi Iye amene akukupempha madzi akumwa, ukanamupempha ndipo
akanakupatsa madzi amoyo.”
11 Mayiyo anati, “Ambuye, Inu mulibe kanthu kotungira madzi ndipo
chitsime ndi chakuya. Kodi madzi amoyowo mungawatenge kuti? 12 Kodi
Inu ndinu wamkulu kuposa kholo lathu Yakobo, amene anatipatsa
chitsimechi ndipo iye ankamwanso monga anachita ana ake ndi ziweto
zake?”
13 Yesu anayankha kuti, “Aliyense amene amamwa madzi awa amam-
vanso ludzu, 14 koma aliyense amene adzamwa madzi amene Ine
ndidzamupatsa sadzamvanso ludzu. Ndithudi, madzi amene ndidzamu-
patsa adzakhala kasupe wamadzi wotumphukira ku moyo wosatha.”
15 Mayiyo anati kwa Iye, “Ambuye, patseni madzi amenewo kuti
ndisadzamvenso ludzu ndi kumabwerabe kuno kudzatunga madzi.”
16 Iye anamuwuza kuti, “Pita kayitane mwamuna wako ndipo ubwere
naye.”
17 Iye anayankha kuti, “Ine ndilibe mwamuna.”
Yesu anati kwa iye, “Wakhoza ponena kuti ulibe mwamuna. 18 Zoona
n’zakuti iwe wakhala pa banja ndi amuna asanu, ndipo mwamuna amene
uli naye tsopano si wako. Zimene wanenazi ndi zoona.”
19 Mayiyo anati, “Ambuye, ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri.
20 Makolo athu ankapembedza m’phiri ili koma inu Ayuda mumati malo
amene tiyenera kupembedzera ali ku Yerusalemu.”
21 Yesu anati, “Mayi inu khulupirira Ine. Nthawi ikubwera pamene
inu simudzapembedza Atate m’phiri ili kapena mu Yerusalemu. 22 Inu
Asamariya mumapembedza chimene simukuchidziwa. Ife timapembedza
chimene tikuchidziwa, pakuti chipulumutso n’chochokera kwa Ayuda.
23 Koma nthawi ikubwera ndipo yafika kale tsopano pamene opembedza
woona adzapembedza Atate mu mzimu ndi m’choonadi, pakuti opem-
bedza otere ndiwo amene Atate akuwafuna. 24 Mulungu ndi Mzimu, ndipo
omupembedza Iye ayenera kumupembedza mu mzimu ndi m’choonadi.”
25 Mayiyo anati, “Ine ndikudziwa kuti Mesiya (wotchedwa Khristu)
akubwera. Akabwera, Iye adzafotokoza zonse kwa ife.”
26 Ndipo Yesu anamuwuza kuti, “Amene ndikukuyankhulane, ndine
amene.”

### *Ophunzira Abweranso kwa Yesu*

27 Pa nthawi yomweyo ophunzira ake anabwerera ndipo anadabwa
kupeza Iye akuyankhula ndi mayi. Koma palibe amene anamufunsa kuti,
“Kodi mukufuna chiyani?” kapena, “N’chifukwa chiyani mukuyankhula
naye?”
28 Kenaka mayiyo anasiya mtsuko wamadzi, nabwerera ku mzinda
ndipo anati kwa anthu, 29 “Tiyeni mukaone munthu amene wandiwuza

ine zilizonse zimene ndinazichita. Kodi ameneyu sangakhale Khristu?”
30 Iwo anatuluka m’mudziwo ndi kupita kumene kunali Iye.

31 Pa nthawi imeneyi ndi kuti ophunzira ake akumukakamiza kuti, “Rabi idyani.”

32 Koma Iye anawawuza kuti, “Ine ndili ndi chakudya choti ndidye chimene inu simukuchidziwa.”

33 Ndipo ophunzira ake anafunsana wina ndi mnzake kuti, “Kodi alipo wina amene anamubweretsera Iye chakudya?”

34 Yesu anati, “Chakudya changa ndikuchita chifuniro cha Iye amene
ananditumia Ine ndi kumaliza ntchito yake.
35 Kodi inu simunena kuti,
‘Kwatsala miyezi inayi ndipo kenaka kukolola?’ Ine ndikukuwuzani kuti,
tsekulani maso anu ndipo muyang’ane m’minda! Mbewu zacha kale kuti
zikololedwe.
36 Ngakhale tsopano amene akukolola akulandira malipiro
ake, ndipo akututa mbewu ku moyo wosatha kuti wofesa ndi wokolola
asangalale pamodzi.
37 N’chifukwa chake mawu akuti, ‘Wina amafesa
ndipo wina amakolola’ ndi woona.
38 Ine ndinakutumani kukakolola
zimene simunagwirire ntchito. Ena anagwira ntchito yolemetsa ndipo inu mwatuta phindu la ntchito yawo.”

### *Asamariya Ambiri Akhulupirira*

39 Asamariya ambiri ochokera m’mudziwo anakhulupirira Iye chifukwa cha umboni wa mayiyo wakuti, “Iye anandiwuza ine zonse ndinazichita.”
40 Choncho Asamariya atabwera kwa Iye, anamuwumiriza Iye kuti akhale
nawo, ndipo Iye anakhala nawo masiku awiri.
41 Ndipo chifukwa cha mawu ake, ena ambiri anakhulupirira.

42 Iwo anati kwa mayiyo, “Ife sitikukhulupirira chifukwa cha mawu ako okha, koma tsopano ife tadzimvera tokha, ndipo tikudziwa kuti munthu uyu ndithu ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi.”

### *Yesu Achiritsa Mwana wa Nduna ya Mfumu*

43 Patatha masiku awiri Iye anachoka napita ku Galileya.
44 (Tsopano Yesu mwini ananena kale kuti mneneri salandira ulemu m’dziko lake).
45 Iye atafika ku Galileya, Agalileya anamulandira. Iwo anali ataona zonse zimene anazichita mu Yerusalemu pa phwando la Paska, pakuti iwonso anali komweko.

46 Iye anakafikanso ku Kana wa ku Galileya, kumene anasanduliza madzi kukhala vinyo. Ndipo kumeneko kunali nduna ina ya mfumu imene mwana wake wamwamuna anali chigonere akudwala ku Kaperenawo.
47 Munthu uyu atamva kuti Yesu wafika ku Galileya kuchokera ku Yudeya, anapita kwa Iye, namupempha kuti apite akachiritse mwana wakeyo, amene anali pafupi kufa.

48 Yesu anawawuza iwo kuti, “Anthu inu pokhapokha mutaona zizindikiro zodabwitsa, simudzakhulupirira.”

49 Nduna ya mfumuyo inati, “Ambuye tiyeni mwana wanga asanafe.”

50 Yesu anayankha kuti, “Pita. Mwana wako adzakhala ndi moyo.”

Munthuyo anakhulupirira mawu a Yesu ndipo ananyamuka.
51 Iye ali pa njira, antchito ake anakumana naye, namuwuza kuti mwana wanu uja
wachira.
52 Iye atafunsa kuti ndi nthawi yanji imene mwana wake anapeza bwino, iwo anati kwa iye, “Malungo anamusiya iye dzulo pa ora lachisanu ndi chiwiri.”

[53] Ndipo bamboyo anazindikira kuti iyi inali nthawi yomweyo imene
Yesu anati kwa iye, "Mwana wako adzakhala ndi moyo." Choncho iye ndi
onse a pa banja lake anakhulupirira.
[54] Ichi ndiye chinali chizindikiro chodabwitsa chachiwiri chimene Yesu
anachita atafika ku Galileya kuchokera ku Yudeya.

# 5

### *Yesu Achiritsa Munthu pa Sabata*

[1] Patapita nthawi Yesu anakwera kupita ku Yerusalemu ku phwando
la Ayuda. [2] Ndipo ku Yerusalemuko pafupi ndi chipata cha Nkhosa kuli
dziwe limene m'Chihebri limatchedwa Betisaida ndipo ndi lozunguliridwa
ndi makumbi asanu. [3] M'menemo munkagonamo gulu lalikulu la anthu
odwala, osaona, olumala ndi ofa ziwalo. [4] Pakuti nthawi zina mngelo
wa Ambuye ankatsikira m'dziwemo n'kuvundula madziwo. Woyamba
kulowamo madzi atavundulidwa, ankachira ngakhale akhale ndi nthenda
yanji. [5] Mmodzi wa amene anali pamenepo anali atadwala zaka 38.
[6] Yesu atamuona ali chigonere, nadziwa kuti anakhala chotero kwa nthawi
yayitali, anamufunsa iye kuti, "Kodi ukufuna kuchira?"
[7] Wodwalayo anayankha kuti, "Ambuye, ndilibe wina aliyense woti
angandithandize kulowa m'dziwe pamene madzi avundulidwa. Pamene
ndikuyesera kuti ndilowemo, wina amalowamo ine ndisanalowemo."
[8] Ndipo Yesu anati kwa iye, "Imirira! Nyamula mphasa yako yamba
kuyenda." [9] Nthawi yomweyo munthuyo anachiritsidwa. Iye ananyamula
mphasa yake nayamba kuyenda.

Tsiku limene izi zinachitika linali la Sabata. [10] Ndipo Ayuda anati kwa
munthu amene anachiritsidwayo, "Lero ndi la Sabata; lamulo silikulola
iwe kunyamula mphasa yako."
[11] Koma iye anayankha kuti, "Munthu amene wandichiritsa anati kwa
ine, 'Nyamula mphasa yako yamba kuyenda.' "
[12] Pamenepo anamufunsa iye kuti, "Kodi munthu ameneyo ndani amene
wakuwuza kuti, 'Nyamula mphasa yako ndipo yenda?' "
[13] Munthu amene anachiritsidwayo sanadziwe kuti anali ndani, pakuti
Yesu anangolowera m'gulu la anthu ndi kupita.
[14] Patapita nthawi Yesu anamupeza ku Nyumba ya Mulungu ndipo
anati kwa iye, "Taona uli bwino tsopano. Usakachimwenso kuti choyipa
choposa ichi chingakugwere." [15] Munthu uja anachoka ndi kukawawuza
Ayuda kuti anali Yesu amene anamuchiritsa iye.

### *Yesu Adziwulula kuti ndi Mwana wa Mulungu*

[16] Ndipo popeza Yesu amachita zinthu izi tsiku la Sabata, Ayuda
anayamba kumulondalonda. [17] Yesu anawawuza kuti, "Atate anga
amagwira ntchito nthawi zonse mpaka lero lino, ndipo Inenso ndili pa
ntchito." [18] Chifukwa cha ichi Ayuda anawirikiza kufuna kumupha;
osati chifukwa chakuswa Sabata kokha komanso chifukwa ankanena kuti
Mulungu ndi Atate ake, nadziyesa Iye wofanana ndi Mulungu.
[19] Yesu anawapatsa yankho ili: "Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti
Mwana sangathe kuchita kanthu pa Iye yekha. Iye amachita zokhazo
zimene amaona Atate ake akuchita, chifukwa chilichonse chimene Atate
amachita Mwana amachitanso. [20] Pakuti Atate amakonda Mwana, ama-
muonetsa zonse zimene Iwo amachita. Inde, Atate adzamuonetsa zinthu
zazikulu kuposa zimenezi ndipo mudzadabwa. [21] Pakuti monga Atate

amaukitsa akufa nawapatsa moyo, momwemonso Mwana amapereka
moyo kwa amene Iye akufuna. 22 Komanso, Atate saweruza aliyense
koma wapereka kwa Mwana ulamuliro woweruzawo, 23 kuti aliyense
alemekeze Mwanayo monga momwe amalemekezera Atate. Munthu
amene salemekeza Mwana salemekezanso Atate amene anamutuma
Mwanayo.

24 "Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti aliyense amene amamva mawu
anga ndi kukhulupirira Iye amene ananditumiza Ine, ali ndi moyo wosatha
ndipo sadzaweruzidwa. Iye wachoka mu imfa ndipo walowa m'moyo.
25 Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti nthawi ikubwera ndipo yafika kale
tsopano, pamene akufa adzamva mawu a Mwana wa Mulungu ndipo iwo
amene amva adzakhala ndi moyo. 26 Pakuti monga Atate ali gwero la
moyo, momwemonso anapereka mphamvu zopereka moyo mwa Mwana.
27 Ndipo wamupatsa Iye ulamuliro woweruza chifukwa ndi Mwana wa
Munthu.

28 "Musadabwe ndi zimenezi. Pakuti nthawi ikubwera pamene onse
amene ali m'manda adzamva mawu ake 29 ndi kutuluka. Iwo amene
anachita zabwino adzauka ndi kupita ku moyo wosatha ndipo amene
anachita zoyipa adzauka ndi kupita ku chilango chamuyaya. 30 Pakuti
sindingathe kuchita kena kalikonse pa ndekha. Ine ndimaweruza
molingana ndi zomwe Mulungu wandiwuza ndipo kuweruza kwanga ndi
kolungama. Ine sindifuna kudzikondweretsa ndekha koma Iye amene
ananditumа.

### *Maumboni Onena za Yesu*

31 "Ngati ndidzichitira umboni ndekha, umboni wanga si woona. 32 Alipo
wina amene amandichitira umboni wabwino. Ine ndikudziwa kuti
umboni wake wonena za Ine ndi woona.

33 "Inu munatumiza amithenga kwa Yohane ndipo iye anachitira
umboni choona. 34 Sikuti Ine ndikudalira umboni wa munthu; koma
ndikunena zimenezi kuti mupulumutsidwe. 35 Yohane anali ngati nyale
imene imayaka ndi kuwala, ndipo inu kwa kanthawi munasankha
kusangalala ndi kuwala kwakeko.

36 "Koma Ine ndili ndi umboni woposa uja wa Yohane. Pakuti ntchito
imene Atate andipatsa kuti ndiyikwaniritse ndi imene ndikugwira, ndipo
ikundichitira umboni kuti Atate anditumа Ine. 37 Ndipo Atate amene anan-
dituma Ine, Iye mwini wandichitira umboni. Inu simunamvepo mawu
ake kapena kuona maonekedwe ake, 38 kapena mawu ake kukhala mwa
inu, pakuti simukhulupirira Iye amene anamutuma. 39 Inu mumasanthula
malemba chifukwa mumaganiza kuti m'malembamo muli moyo wosatha.
Awa ndi malemba amene akundichitira umboni. 40 Koma inu mukukana
kubwera kwa Ine kuti mukhale ndi moyo.

41 "Ine sindilandira ulemu kuchokera kwa anthu 42 koma Ine
ndikukudziwani. Ndikudziwa kuti m'mitima mwanu mulibe chikondi
cha Mulungu. 43 Ine ndabwera m'dzina la Atate anga, ndipo inu
simukundirandira Ine; koma wina wake akabwera m'dzina la iye mwini,
inu mudzamulandira. 44 Kodi inu mudzakhulupirira bwanji ngati
mumapatsana ulemu wina ndi mnzake, ndipo simufuna kulandira ulemu
kuchokera kwa Mulungu yekhayo?

45 "Koma inu musaganize kuti Ine ndidzakunenezani kwa Atate.
Wokunenezani ndi Mose, amene inu mwayikapo chiyembekezo chanu.
46 Ngati mukanakhulupirira Mose, mukanakhulupiriranso Ine, pakuti iye

analemba za Ine. 47 Koma ngati simukhulupirira zimene iye analemba,
mudzakhulupirira bwanji zimene Ine ndikunena?"

# 6

### *Yesu Adyetsa Anthu 5,000*

1 Nthawi ina zitatha izi, Yesu anawolokera ku gombe la kutali la
nyanja ya Galileya (iyi ndi nyanja ya Tiberiya), 2 ndipo gulu lalikulu la
anthu linamutsata Iye chifukwa linaona zizindikiro zodabwitsa zimene
anazichita pa odwala. 3 Kenaka Yesu anakwera pa phiri nakhala pansi ndi
ophunzira ake. 4 Tsopano phwando la Paska la Ayuda linali pafupi.

5 Yesu atakweza maso ndi kuona gulu lalikulu la anthu likubwera
kwa Iye, anati kwa Filipo, "Kodi tingagule kuti buledi kuti anthu awa
adye?" 6 Iye anafunsa izi kumuyesa chabe, pakuti Iye ankadziwa chimene
ankayenera kuchita.

7 Filipo anamuyankha Iye kuti, "Malipiro a miyezi isanu ndi itatu
sangathe kugula buledi okwanira aliyense kuti adye!"

8 Mmodzi wa ophunzira ake, Andreya, m'bale wa Simoni Petro, anati,
9 "Pano pali mnyamata amene ali ndi buledi musanu wabarele ndi
tinsomba tiwiri, kodi zingakwane onsewa?"

10 Yesu anati, "Awuzeni anthuwa akhale pansi." Pamalo pamenepa
panali udzu wambiri ndipo amuna amene anakhala pansi anali osachep-
era 5,000. 11 Kenaka Yesu anatenga bulediyo, atayamika anagawira iwo
amene anakhala pansi, chimodzimodzinso nsombazo monga momwe iwo
anafunira.

12 Ndipo atakhuta, Iye anati kwa ophunzira ake, "Tolani zotsala kuti
pasawonongeke kanthu." 13 Choncho iwo anasonkhanitsa makombo
nadzaza madengu khumi ndi awiri.

14 Pambuyo pake anthu ataona chizindikiro chodabwitsa chimene Yesu
anachita, iwo anati, "Zoonadi uyu ndi Mneneri wakudzayo m'dziko la
pansi." 15 Yesu atadziwa kuti iwo amafuna kubwera kudzamuwumiriza
kuti akhale mfumu, anachoka napita ku phiri pa yekha.

### *Yesu Ayenda pa Madzi*

16 Pofika madzulo, ophunzira ake anatsikira ku nyanja, 17 kumene
iwo analowa m'bwato ndi kuyamba kuwoloka nyanja kupita ku Kaper-
enawo. Tsopano kunali kutada ndipo Yesu anali asanabwerere kwa iwo.
18 Mphepo yamphamvu inawomba ndipo nyanja inalusa. 19 Iwo atayenda
makilomita asanu kapena asanu ndi limodzi, anaona Yesu akuyandikira
bwatolo, akuyenda pa madzi; ndipo anachita mantha. 20 Koma Iye
anawawuza kuti, "Ndine, musaope." 21 Ndipo iwo analola kumutenga
m'bwatomo, nthawi yomweyo bwatolo linafika ku gombe la nyanja
kumene ankapita.

22 Pa tsiku lotsatira gulu la anthu limene linatsala kumbali ina yanyan-
jayo linaona kuti panali bwato limodzi lokha, ndipo kuti Yesu sanalowe
m'bwatomo pamodzi ndi ophunzira ake, koma kuti ophunzirawo anapita
okha. 23 Kenaka mabwato ena ochokera ku Tiberiya anafika pafupi ndi
pamalo pamene anthu anadya buledi Ambuye atayamika. 24 Nthawi
yomwe gulu la anthu linaona kuti Yesu kapena ophunzira ake sanali
pamenepo, ilo linalowanso m'mabwatowo ndi kupita ku Kaperenawo
kukamufunafuna Yesu.

### *Yesu Chakudya Chamoyo*

25 Atamupeza mbali ina ya nyanjayo, iwo anamufunsa Iye kuti, “Rabi,
mwafika nthawi yanji kuno?”
26 Yesu anawayankha kuti, “Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti mukun-
difuna, osati chifukwa munaona zizindikiro zodabwitsa koma chifukwa
munadya chakudya ndi kukhuta. 27 Gwirani ntchito, osati chifukwa
cha chakudya chimene chimawonongeka koma chifukwa cha chakudya
chimene sichiwonongeka mpaka ku moyo wosatha, chimene Mwana
wa Munthu adzakupatsani. Mulungu Atate anamusindikiza chizindikiro
chomuvomereza.”
28 Kenaka anamufunsa Iye kuti, “Kodi tichite chiyani kuti tigwire ntchito
za Mulungu?”
29 Yesu anayankha kuti, “Ntchito ya Mulungu ndi iyi: Kukhulupirira Iye
amene anamutuma.”
30 Choncho iwo anamufunsa Iye kuti, “Kodi mudzatipatsa chizindikiro
chodabwitsa chotani kuti ife tichione ndi kukhulupirira Inu? Kodi
mudzachita chiyani? 31 Makolo athu akale anadya mana m’chipululu;
monga zalembedwa: ‘anawapatsa buledi wochokera kumwamba kuti
adye.’ ”
32 Yesu anawawuza kuti, “Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti si Mose
amene ankakupatsani chakudya chochokera kumwamba, koma ndi Atate
anga amene ankakupatsani chakudya chenicheni chochokera kumwamba.
33 Pakuti chakudya cha Mulungu ndi Iye amene wabwera kuchokera
kumwamba ndi kupereka moyo ku dziko la pansi.”
34 Iwo anati, “Ambuye, kuyambira tsopano muzitipatsa buledi
ameneyu.”
35 Kenaka Yesu ananenetsa kuti, “Ine ndine chakudya chamoyo. Iye
amene abwera kwa Ine sadzamva njala, ndipo iye amene akhulupirira Ine
sadzamva ludzu. 36 Monga ndakuwuzani kale, ngakhale kuti mwandiona
simukukhulupirirabe. 37 Zonse zimene Atate andipatsa zidzabwera kwa
Ine, ndipo aliyense amene adzabwera kwa Ine sindidzamutaya kunja.
38 Pakuti Ine ndinatsika kuchokera kumwamba osati kudzachita chifuniro
changa koma cha Iye amene ananditumа Ine. 39 Ndipo chifuniro cha
Iye amene ananditumа Ine n’chakuti ndisatayepo ngakhale ndi mmodzi
yemwe mwa onse amene Iye wandipatsa, koma kuti ndidzawaukitse
kwa akufa pa tsiku lomaliza. 40 Pakuti chifuniro cha Atate anga ndi
chakuti aliyense amene aona Mwanayo namukhulupirira akhale ndi moyo
wosatha, ndipo Ine ndidzamuukitsa kwa akufa pa tsiku lomaliza.”
41 Pamenepo Ayuda anayamba kung’ung’udza chifukwa anati, “Ine
ndine chakudya chotsika kuchokera kumwamba.” 42 Iwo anati, “Kodi
uyu si Yesu, mwana wa Yosefe, amene abambo ake ndi amayi ake
timawadziwa? Nanga Iyeyu akunena bwanji kuti, ‘Ine ndinatsika
kuchokera kumwamba?’ ”
43 Yesu anayankha kuti, “Musang’ung’udze pakati panu.” 44 Palibe
munthu amene angabwere kwa Ine, ngati Atate amene ananditumа Ine
samubweretsa. Ndipo Ine ndidzamuukitsa kwa akufa pa tsiku lomaliza.
45 Aneneri analemba kuti, “Onse adzaphunzitsidwa ndi Mulungu! Aliyense
amene amamva Atate ndi kuphunzira kwa Iye amabwera kwa Ine.
46 Palibe amene anaona Atate koma yekhayo amene achokera kwa
Mulungu; yekhayo ndiye anaona Atate. 47 Zoonadi, Ine ndikukuwuzani
kuti Iye amene akhulupirira ali nawo moyo wosatha. 48 Ine ndine

chakudya chamoyo. 49 Makolo anu akale anadya mana m'chipululu,
komabe anafa. 50 Koma pano pali chakudya chochokera kumwamba,
chimene munthu akadya sangafe. 51 Ine ndine chakudya chamoyo
chochokera kumwamba. Ngati munthu adya chakudya ichi, adzakhala
ndi moyo nthawi zonse. Chakudya chimenechi ndi thupi langa, limene
Ine ndidzalipereka kuti anthu pa dziko lapansi akhale ndi moyo."
52 Kenaka Ayuda anayamba kutsutsana kwambiri pakati pawo kuti,
"Kodi munthu uyu angathe kutipatsa bwanji thupi lake kuti tidye?"
53 Yesu anawawuza kuti, "Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti ngati
simungadye thupi la Mwana wa Munthu ndi kumwa magazi ake,
simungakhale ndi moyo mwa inu. 54 Aliyense amene adya thupi langa ndi
kumwa magazi anga ali ndi moyo wosatha ndipo Ine ndidzamuukitsa kwa
akufa pa tsiku lomaliza. 55 Pakuti thupi langa ndi chakudya chenicheni
ndipo magazi anga ndi chakumwa chenicheni. 56 Aliyense amene adya
thupi langa ndi kumwa magazi anga amakhala mwa Ine, ndi Ine mwa iye.
57 Monga Atate amoyo ananditurna Ine, ndipo ndili ndi moyo chifukwa
cha Atatewo, chomwechonso amene adya thupi langa adzakhala ndi moyo
chifukwa cha Ine. 58 Ichi ndiye chakudya chimene chinatsika kuchokera
kumwamba. Makolo athu akale anadya mana ndi kufa, koma iye amene
adya chakudya ichi, adzakhala ndi moyo nthawi yonse." 59 Iye ankanena
izi pamene ankaphunzitsa m'sunagoge mu Kaperenawo.

### *Ophunzira Ambiri Aleka Kutsata Yesu*

60 Pakumva izi ambiri a ophunzira ake anati, "Ichi ndi chiphunzitso
chovuta. Angachilandire ndani?"
61 Pozindikira kuti ophunzira ake ankang'ung'udza, Yesu anawafunsa
kuti, "Kodi izi zikukukhumudwitsani? 62 Nanga mutaona Mwana wa
Munthu akukwera kupita kumene Iye anali poyamba! 63 Mzimu Woyera
apereka moyo, thupi silipindula kanthu. Mawu amene ndayankhula kwa
inu ndiwo mzimu ndipo ndi moyo. 64 Komabe alipo ena mwa inu amene
sakukhulupirira." Pakuti Yesu ankadziwa kuyambira pachiyambi ena
mwa iwo amene samakhulupirira ndi amene adzamupereka Iye. 65 Iye
anapitiriza kunena kuti, "Ichi ndi chifukwa chake ndinakuwuzani kuti
palibe wina angabwere kwa Ine pokhapokha Atate atamuthandiza."
66 Kuyambira nthawi imeneyi ophunzira ake ambiri anabwerera ndipo
sanamutsatenso Iye.
67 Yesu anafunsa khumi ndi awiriwo kuti, "Kodi inu mukufuna ku-
chokanso?"
68 Simoni Petro anamuyankha Iye kuti, "Ambuye, ife tidzapita kwa yani?
Inu muli ndi mawu amoyo wosatha. 69 Ife tikhulupirira ndi kudziwa kuti
Inu ndinu Woyerayo wa Mulungu."
70 Kenaka Yesu anayankha kuti, "Kodi Ine sindinakusankheni inu khumi
ndi awiri? Komabe mmodzi wa inu ndi mdierekezi." 71 (Iye amanena
Yudasi, mwana wa Simoni Isikarioti amene ngakhale anali mmodzi mwa
khumi ndi awiriwo, anali woti adzamupereka).

## 7

### *Yesu Apita Kuphwando Lamisasa*

1 Zitatha izi Yesu anayendayenda mu Galileya, ndi cholinga chakuti
asafike ku Yudeya chifukwa Ayuda kumeneko amadikira kuti amuphe.
2 Koma phwando la Ayuda lamisasa litayandikira, 3 abale a Yesu anati kwa

Iye, “Inu muyenera kuchoka kuno ndi kupita ku Yudeya, kuti ophunzira
anu akaone zodabwitsa zomwe mumachita. 4 Palibe wina aliyense
amene amafuna kukhala wodziwika amachita zinthu mseri. Popeza Inu
mukuchita zinthu izi, mudzionetsere nokha ku dziko la pansi.” 5 Pakuti
ngakhale abale ake omwe sanamukhulupirire.

6 Choncho Yesu anawawuza iwo kuti, “Nthawi yanga yoyenera sinafike;
kwa inu nthawi ina iliyonse ndi yoyenera. 7 Dziko lapansi silingakudeni
inu, koma limandida Ine chifukwa Ine ndimachitira umboni kuti zomwe
limachita ndi zoyipa. 8 Inu pitani kuphwando. Ine sindipita tsopano
kuphwando ili chifukwa kwa Ine nthawi yoyenera sinafike.” 9 Atanena
izi, Iye anakhalabe mu Galileya.

10 Komabe, abale ake atanyamuka kupita kuphwando, Iye anapitanso,
osati moonekera, koma mseri. 11 Tsopano kuphwandoko Ayuda anakamu-
funafuna ndi kumafunsana kuti, “Kodi munthu ameneyu ali kuti?”

12 Pakuti pa chigulu cha anthu panali kunong’ona ponseponse za Iye.
Ena ankanena kuti, “Iye ndi munthu wabwino.”

Ena ankayankha kuti, “Ayi, Iye amanamiza anthu.” 13 Koma panalibe
amene ankanena kalikonse poyera za Iye chifukwa choopa Ayuda.

### *Yesu Aphunzitsa pa Phwando*

14 Phwando lili pakatikati, Yesu anapita ku bwalo la Nyumba ya Mulungu
ndi kuyamba kuphunzitsa. 15 Ayuda anadabwa ndipo anafunsa kuti, “Kodi
munthu uyu nzeru izi anazitenga kuti popanda kuphunzira?”

16 Yesu anayankha kuti, “Chiphunzitso changa si cha Ine ndekha.
Chimachokera kwa Iye amene ananditumа. 17 Ngati munthu asankha
kuchita chifuniro cha Mulungu, adzazindikira ngati chiphunzitso changa
n’chochokera kwa Mulungu kapena ngati ndi mwa Ine ndekha. 18 Iye
amene amayankhula za Iye mwini amatero kuti adzipezere ulemu,
koma amene amagwira ntchito kuti amene anamutuma alandire ulemu,
ameneyo ndiye munthu woona; mu mtima mwake mulibe chinyengo
chilichonse. 19 Kodi Mose sanakupatseni lamulo? Komatu palibe ndi
mmodzi yemwe mwa inu amene akusunga lamulo. N’chifukwa chiyani
mukufuna kundipha Ine?”

20 Gulu la anthu linayankha kuti, “Iwe ndiye wagwidwa ndi ziwanda.
Ndani akufuna kukupha?”

21 Yesu anawawuza kuti, “Ine ndinachita chodabwitsa chimodzi ndipo
inu mwadabwa. 22 Koma, chifukwa chakuti Mose anakulamulani kuti
muzichita mdulidwe (ngakhale kuti sunachokere kwa Mose, koma kwa
makolo anu), inuyo mumachita mdulidwe mwana tsiku la Sabata.
23 Tsopano ngati mwana angachite mdulidwe pa Sabata kuti lamulo la
Mose lisaswedwe, n’chifukwa chiyani mukundipsera mtima chifukwa
chochiritsa munthu pa Sabata? 24 Musamaweruze potengera maonekedwe
chabe, koma weruzani molungama.”

### *Kodi Yesu ndi Khristu?*

25 Pa nthawi imeneyi anthu ena a ku Yerusalemu anayamba kufunsana
kuti, “Kodi uyu si munthu uja akufuna kumuphayu? 26 Uyu ali apa,
kuyankhula poyera, ndipo iwo sakunena kanthu kwa Iye. Kodi olamulira
atsimikizadi kuti Iye ndi Khristu? 27 Koma ife tikudziwa kumene achokera
munthuyu; pamene Khristu adzabwere, palibe amene adzadziwa kumene
akuchokera.”

28 Kenaka Yesu, akuphunzitsabe m'bwalo la Nyumba ya Mulungu
anafuwula kuti, "Zoona, mukundidziwa Ine, ndipo mukudziwa kumene
ndikuchokera. Ine sindili pano mwa Ine ndekha, koma Iye amene anan-
dituma Ine ndi woona. Inu simukumudziwa, 29 koma Ine ndikumudziwa
chifukwa ndichokera kwa Iyeyo ndipo ndiye amene ananditumа Ine."

30 Chifukwa cha izi iwo anayesa kumugwira Iye, koma palibe aliyense
amene anayika dzanja lake pa Iye, chifukwa nthawi yake inali isanafike.
31 Komabe, ambiri a m'chigulucho anamukhulupirira Iye. Iwo anati, "Kodi
pamene Khristu abwera, adzachita zizindikiro zodabwitsa zambiri kuposa
munthu uyu?"

32 Afarisi anamva chigulucho chikunong'ona zinthu zotere za Iye.
Kenaka akulu a ansembe ndi Afarisi anatumiza asilikali a m'Nyumba ya
Mulungu kuti akamumange Iye.

33 Yesu anati, "Ine ndili ndi inu kwa kanthawi kochepa chabe, ndipo ke-
naka ndizipita kwa Iye amene ananditumа Ine. 34 Inu mudzandifunafuna
koma simudzandipeza; ndipo kumene Ine ndili inu simungathe kubwera."

35 Ayuda anati kwa wina ndi mnzake, "Kodi munthu uyu akuganizira
zoti apite kuti kumene ife sitingathe kumupeza Iye? Kodi Iye adzapita
kumene anthu amakhala mobalalikana pakati pa Agriki, ndi kuphunzitsa
Agriki? 36 Kodi Iye amatanthauza chiyani pamene anati, 'Inu mudzandi-
funafuna koma simudzandipeza,' ndi 'Kumene Ine ndili, inu simungathe
kubwera?' "

### *Mitsinje ya Madzi Opatsa Moyo*

37 Pa tsiku lomaliza ndi lalikulu kwambiri laphwando, Yesu anayimirira
nafuwula nati, "Ngati munthu ali ndi ludzu, abwere kwa Ine kuti
adzamwe. 38 Malemba kuti 'Aliyense amene akhulupirira Ine, mitsinje
yamadzi amoyo idzatuluka kuchokera m'kati mwake.' " 39 Ponena izi Iye
amatanthauza Mzimu Woyera, amene adzalandire amene amakhulupirira
Iye. Pa nthawiyi n'kuti Mzimu Woyera asanaperekedwe, pakuti Yesu anali
asanalemekezedwe.

40 Pakumva mawu ake, ena a anthuwo anati, "Zoonadi munthu uyu ndi
mneneri."

41 Ena anati, "Iye ndiye Khristu."

Komanso ena anafunsa kuti, "Kodi Khristu angachokere bwanji ku
Galileya? 42 Kodi Malemba samanena kuti Khristu adzachokera m'banja
la Davide, ndi ku Betelehemu mu mzinda umene Davide anakhalamo?"
43 Kotero anthu anagawikana chifukwa cha Yesu. 44 Ena anafuna
kumugwira Iye, koma palibe amene anayika dzanja pa Iye.

### *Kusakhulupirira kwa Atsogoleri a Ayuda*

45 Pomaliza asilikali a m'Nyumba ya Mulungu anabwerera kwa akulu
a ansembe ndi Afarisi amene anawafunsa iwo kuti, "Kodi ndi chifukwa
chiyani simunamugwire Iye?"

46 Asilikali aja anati, "Palibe wina amene anayankhula ngati Munthu
ameneyo n'kale lonse."

47 Afarisi anawadzudzula nati, "Kodi mukutanthauza kuti Iye anaku-
namizani inunso?" 48 "Kodi alipo ena a olamulira kapena a Afarisi,
anamukhulupirira Iye? 49 Ayi! Koma gulu limene silidziwa malamulo ndi
lotembereredwa."

50 Nekodimo, amene anapita kwa Yesu poyamba paja ndipo anali
mmodzi wa iwo, anafunsa kuti, 51 “Kodi lamulo lathu limatsutsa munthu
popanda kumva mbali yake kuti tipeze chimene wachita?”
52 Iwo anayankha kuti, “Kodi ndiwenso wochokera ku Galileya?
Tayang’ananso, ndipo udzapeza kuti mneneri sachokera ku Galileya.”

*[Mipukutu yoyambirira ndi maumboni akale mulibe 7:53 mpaka 8:11]*

### *Za Mkazi Wachigololo*

53 Kenaka onse anachoka, napita kwawo.

## 8

1 Koma Yesu anapita ku phiri la Olivi. 2 Mmamawa Iye anaonekeranso
ku Nyumba ya Mulungu kumene anthu onse anamuzungulira ndipo Iye
anakhala pansi nawaphunzitsa. 3 Aphunzitsi amalamulo ndi Afarisi anab-
weretsa mkazi amene anagwidwa akuchita chigololo. Iwo anamuyimiritsa
patsogolo pa anthu ndipo 4 anati kwa Yesu, “Aphunzitsi, mkazi uyu
tinamugwira akuchita chigololo. 5 M’malamulo a Mose anatilamulira
kuti akazi otere tiwagende ndi miyala. Tsopano Inu mukuti chiyani?”
6 Iwo anagwiritsa ntchito funsoli ngati msampha, ndi cholinga choti apeze
chifukwa cha kumuneneza Iye.
Koma Yesu anawerama pansi ndi kuyamba kulemba pa dothi ndi chala
chake. 7 Pamene iwo anapitirira kumufunsa, Iye anaweramuka ndipo
anawawuza kuti, “Ngati wina wa inu alipo wopanda tchimo, ayambe iyeyo
kumugenda ndi miyala mkaziyu.” 8 Iye anaweramanso pansi ndi kulemba
pa dothi.
9 Iwo atamva izi anayamba kuchoka mmodzimmodzi, akuluakulu
poyamba, mpaka Yesu anatsala yekha ndi mkaziyo atayimirira pomwepo.
10 Yesu anaweramuka ndipo anamufunsa iye kuti, “Akuluakulu aja ali
kuti? Kodi palibe amene wakutsutsa?”
11 Iye anati, “Ambuye, palibe ndi mmodzi yemwe.”
“Inenso sindikukutsutsa iwe. Pita kuyambira tsopano
usakachimwenso.”

### *Za Umboni wa Yesu*

12 Yesu atayankhulanso kwa anthu, anati, “Ine ndine kuwunika kwa
dziko lapansi. Aliyense amene anditsata Ine sadzayenda mu mdima, koma
adzakhala ndi kuwala kotsogolera anthu ku moyo.”
13 Afarisi anamutsutsa Iye nati, “Iwe ukudzichitira umboni wa Iwe
mwini, umboni wako siwoona.”
14 Yesu anayankha kuti, “Ngakhale Ine ndidzichitire umboni, umboni
wangawu ndi woona, pakuti Ine ndikudziwa kumene ndinachokera ndi
kumene ndikupita. Koma inu simukudziwa ndi pang’ono pomwe kumene
ndinachokera kapena kumene ndikupita. 15 Inu mumaweruza potsata
maganizo a anthu chabe. Ine sindiweruza munthu wina aliyense. 16 Koma
Ine ndikati ndiweruze, ndimaweruza molondola, chifukwa Ine sindili
ndekha koma ndili ndi Atate amene anandituma. 17 M’malamulo anu
munalembedwa kuti umboni wa anthu awiri ndi wovomerezeka. 18 Ine
ndikudzichitira ndekha umboni; ndipo mboni inanso ndi Atate amene
anandituma.”
19 Kenaka iwo anamufunsa Iye kuti, “Kodi Atate anuwo ali kuti?”
Yesu anayankha kuti, “Inu simundidziwa Ine. Atate anganso
simuwadziwa. Mukanandidziwa Ine, mukanawadziwanso Atate anga.”

20 Iye anayankhula mawu awa pamene amaphunzitsa Nyumba ya Mu-
lungu pafupi ndi malo amene amaponyapo zopereka. Komabe palibe
amene anamugwira Iye, chifukwa nthawi yake inali isanakwane.

### *Mkangano Woti Yesu Ndani*

21 Kenakanso Yesu anawawuza kuti, "Ine ndikupita, ndipo mudzandi-
funafuna, koma mudzafa muli m'machimo anu. Kumene ndikupita, inu
simungabwereko."
22 Izi zinachititsa Ayuda kufunsa kuti, "Kodi adzadzipha yekha? Kodi
ndicho chifukwa chake akuti, 'Kumene ndikupita, inu simungabwereko?' "
23 Koma Iye anapitiriza kuti, "Inu ndi ochokera pansi pano. Ine ndine
wochokera kumwamba. Inu ndinu anthu a dziko la pansi. Ine sindine wa
dziko lapansi lino. 24 Ine ndinakuwuzani kuti mudzafera m'machimo anu
ngati simukhulupirira kuti Ine Ndine. Ndithu inu mudzafera m'machimo
anu."
25 Iwo anafunsa kuti, "Ndinu ndani?"
Yesu anayankha kuti, "Monga Ine ndakhala ndikunena nthawi yonseyi,
26 ndili ndi zambiri zoti ndinene zoweruza inu. Koma Iye amene
ananditumа ndi woona, ndipo chimene Ine ndamva kuchokera kwa Iye,
ndi chimene ndimaliwuza dziko lapansi."
27 Iwo sanazindikire kuti Iye amawawuza za Atate ake. 28 Choncho Yesu
anati, "Inu mukadzapachika Mwana wa Munthu, pamenepo mudzadziwa
kuti Ine Ndine. Mudzadziwa kuti sindichita kalikonse pa Ine ndekha
koma ndimayankhula zokhazo zimene Atate anandiphunzitsa. 29 Iye
amene ananditumа Ine ali nane pamodzi. Iye sanandisiye ndekha popeza
nthawi zonse ndimachita zomwe zimamukondweretsa Iye." 30 Pamene Iye
ankayankhula zimenezi, ambiri anamukhulupirira.

### *Ana a Abrahamu*

31 Kwa Ayuda amene anamukhulupirira, Yesu anati, "Ngati inu mutsatira
chiphunzitso changa, ndithu ndinu ophunzira anga. 32 Tsono mudzadziwa
choonadi, ndipo choonadicho chidzakumasulani."
33 Iwo anamuyankha Iye kuti, "Ife ndife zidzukulu za Abrahamu ndipo
sitinakhalepo akapolo a wina aliyense. Kodi mukunena bwanji kuti, 'Ife
tidzamasulidwa?' "
34 Yesu anayankha kuti, "Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti aliyense
wochita tchimo ndi kapolo wa tchimolo. 35 Pajatu kapolo alibe malo
wokhazikika m'banja, koma mwana ndi wa m'banjamo nthawi zonse.
36 N'chifukwa chake ngati Mwana adzakumasulani, mudzakhala mfulu
ndithu. 37 Ine ndikudziwa kuti inu ndinu zidzukulu za Abrahamu.
Chonsecho inu mwakonzeka kundipha Ine, chifukwa mawu anga alibe
malo mwa inu. 38 Ine ndikukuwuzani zimene ndaziona pamaso pa Atate,
ndipo inu mukuchita zimene mwazimva kwa abambo anu."
39 Iwo anayankha kuti, "Ife abambo athu ndi Abrahamu."
Yesu anati, "Inu mukanakhala ana a Abrahamu, bwenzi mukuchita
zinthu zimene Abrahamuyo ankachita. 40 Koma mmene zililimu, inu
mwatsimikiza kundipha Ine, munthu amene ndinakuwuzani choonadi
chimene Ine ndinachimva kuchokera kwa Mulungu. Abrahamu sanachite
zinthu zoterezi. 41 Inu mukuchita zinthu zimene abambo anu amachita."
Iwo anatsutsa kuti, "Ife si ana am'chigololo, Atate amene tili nawo ndi
Mulungu yekha."

### *Ana a Mdierekezi*

42 Yesu anawawuza kuti, “Mulungu akanakhala Atate anu, inu
mukanandikonda Ine, pakuti Ine ndinachokera kwa Mulungu ndipo
tsopano ndili pano. Ine sindinabwere mwa Ine ndekha. 43 N’chifukwa
chiyani simukumvetsetsa mawu anga? Chifukwa chake n’chakuti
simungathe kumva zoyankhula zanga. 44 Inu ndinu ana a mdierekezi.
Iye ndiye abambo anu ndipo mukufuna kuchita zimene abambo anuwo
amakhumba. Iye anali wakupha kuyambira pachiyambi, sanasunge
choonadi, pakuti mwa iye mulibe choonadi. Pamene Iye anena bodza,
amayankhula chiyankhulo chobadwa nacho, popeza ndi wabodza ndipo
ndi bambo wa mabodza. 45 Koma chifukwa ndikuwuzani choonadi,
inu simukundikhulupirira Ine! 46 Ndani mwa inu angatsimikize kuti
ndine wochimwa? Ngati Ine ndikunena choonadi, n’chifukwa chiyani
simukundikhulupirira? 47 Munthu wochokera kwa Mulungu amamva
zimene Mulungu amanena. Chifukwa chimene simumvera n’chakuti,
inuyo sindinu ochokera kwa Mulungu.”

### *Zomwe Yesu Ananena za Iye Mwini*

48 Ayuda anamuyankha Iye kuti, “Kodi ife sitikulondola ponena kuti Inu
ndi Msamariya ndi wogwidwa ndi chiwanda?”

49 Yesu anati, “Ine sindinagwidwe ndi chiwanda, koma ndimalemekeza
Atate anga, koma inu mukundinyoza. 50 Ine sindidzifunira ndekha ulemu;
koma alipo wina amene amandifunira, ndipo Iyeyo ndiye woweruza.
51 Ine ndikukuwuzani choonadi, munthu akasunga mawu anga, sadzafa
konse.”

52 Pamenepo Ayuda anafuwula kuti, “Tsopano ife tadziwadi kuti Inu ndi
wogwidwa ndi chiwanda! Abrahamu anafa ndiponso aneneri, koma Inu
mukunena kuti, ‘Ngati munthu asunga mawu anga, sadzafa.’ 53 Kodi ndinu
wa mkulu kuposa abambo athu Abrahamu? Iye anafa, ndiponso aneneri
onse. Inu mukuganiza kuti ndinu yani?”

54 Yesu anayankha kuti, “Ngati Ine ndidzilemekeza ndekha, ulemu
wangawo ndi wosatanthauza kanthu. Atate anga amene inu mukuti ndi
Mulungu wanu, ndiye amene amandilemekeza Ine. 55 Ngakhale kuti
inuyo simukumudziwa, Ineyo ndikumudziwa. Ngati Ine nditanena kuti
sindikumudziwa, Ineyo nditha kukhala wabodza ngati inuyo, koma Ine
ndimamudziwa ndipo ndimasunga mawu ake. 56 Abambo anu Abrahamu
anakondwera poyembekezera kubwera kwanga. Iwo anandiona ndipo
anasangalala.”

57 Ayuda anati kwa Iye, “Inu sumunafike n’komwe zaka makumi asanu,
ndipo mukuti munamuona Abrahamu!”

58 Yesu anayankha kuti, “Ine ndikukuwuzani choonadi, Abrahamu
asanabadwe, Ine Ndine!” 59 Pamenepo iwo anatola miyala kuti amugende,
koma Yesu anabisala, nachoka mozemba m’Nyumba ya Mulungu.

# 9

### *Yesu Achiritsa Munthu Wosaona Chibadwire*

1 Iye akuyendabe, anaona munthu wosaona chibadwire. 2 Ophunzira
ake anamufunsa Iye kuti, “Rabi anachimwa ndani, munthuyu kapena
makolo ake, kuti iye abadwe wosaona?”

3 Yesu anayankha kuti, “Sikuti iyeyu anachimwa kapena makolo ake,
koma izi zinachitika kuti Mulungu aonetse ntchito zake mwa iyeyu. 4 Ife
tiyenera kugwira ntchito za Iye amene anandituma kukanali masana.

Usiku ukubwera, pamene wina aliyense sadzagwira ntchito. 5 Pamene
Ine ndili m'dziko lapansi, Ine ndine kuwunika kwa dziko lapansi."

6 Atanena izi, Iye anathira malovu pansi ndi kukanda dothi, napaka
matopewo m'maso a munthuyo. 7 Yesu anamuwuza iye kuti, "Pita
kasambe m'dziwe la Siloamu" (mawu awa akutanthauza Wotumidwa).
Choncho munthuyo anapita ndi kukasamba ndipo anabwerako akupenya.

8 Anzake ndi iwo amene anamuona iye poyamba akupempha anafunsa
kuti, "Kodi uyu si munthu amene amapemphapempha uja?" 9 Ena
ananena kuti anali yemweyo.

Ena anati, "Ayi, sakuoneka ngati yemweyo."

Koma iye mwini ananenetsa kuti, "Munthuyo ndine."

10 Iwo anafunsitsa kuti, "Kodi nanga maso ako anatsekuka bwanji?"

11 Iye anayankha kuti, "Munthu wina wotchedwa Yesu anakanda dothi
ndi kupaka m'maso anga. Iye anandiwuza kuti ndipite ku Siloamu ndi
kukasamba. Choncho ndinapita kukasamba, ndipo ndikuona."

12 Iwo anamufunsa iye kuti, "Ali kuti munthu ameneyu?"

Iye anati, "Ine sindikudziwa."

### *Afarisi Afufuza za Kuchiritsidwa Kwake*

13 Iwo anabwera naye munthu amene poyamba anali wosaona kwa
Afarisi. 14 Tsono linali la Sabata tsiku limene Yesu anakanda dothi
ndi kutsekula maso a munthuyu. 15 Choncho Afarisi anamufunsanso
iye momwe analandirira kuona kwake. Munthuyo anayankha kuti,
"Iye anapaka matope m'maso anga, ndipo ine ndinakasamba, ndipo
ndikuona."

16 Ena a Afarisi anati, "Munthu uyu siwochokera kwa Mulungu, pakuti
sasunga Sabata."

Koma enanso anafunsa kuti, "Kodi munthu wochimwa angachite bwanji
zizindikiro zodabwitsa ngati izi?" Choncho iwo anagawanika.

17 Pomaliza iwo anatembenukiranso kwa munthu amene anali wosaona
uja nati, "Kodi iwe unena chiyani za Iye poti ndi maso ako amene
watsekula?"

Munthuyo anayankha kuti, "Iye ndi mneneri."

18 Ayuda sanakhulupiririrebe kuti iye anali wosaona ndi kuti anayamba
kuona kufikira atayitana makolo ake. 19 Iwo anafunsa kuti, "Kodi uyu ndi
mwana wanu? Kodi iyeyu ndi amene mukunena kuti anabadwa wosaona?
Nanga zikutheka bwanji kuti akuona?"

20 Makolo anayankha kuti, "Ife tikudziwa kuti ndi mwana wathu, ndipo
tikudziwa kuti anabadwa wosaona. 21 Koma sitidziwa zimene zachi-
tika kuti tsopano azipenya. Amenenso wamupenyetsa sitikumudziwa.
Mufunseni ndi wamkulu; iye adziyankhira yekha." 22 Makolo ake
ananena izi chifukwa amaopa Ayuda, popeza Ayuda anatsimikiza kale kuti
aliyense amene adzamuvomereza Yesu kuti anali Khristu adzatulutsidwa
m'sunagoge. 23 Ichi ndi chifukwa chake makolo ake anati, "Mufunseni iye
ndi wamkulu."

24 Iwo anamuyitanitsa kachiwiri munthu amene anali wosaonayo.
Iwo anati, "Lemekeza Mulungu. Ife tikudziwa kuti munthu uyu ndi
wochimwa."

25 Iye anayankha kuti, "Zakuti Iye ndi wochimwa kapena ayi, ine
sindikudziwa. Ine ndikudziwa chinthu chimodzi. Ndinali wosaona koma
tsopano ndikuona!"

26 Kenaka anamufunsa kuti, “Kodi Iye anachita chiyani kwa iwe? Iye
anatsekula motani maso ako?”
27 Iye anayankha kuti, “Ine ndakuwuzani kale ndipo inu simunamvet-
setse. Chifukwa chiyani mukufuna mumvenso? Mukufuna kuti inu
mukhale ophunzira akenso?”
28 Pamenepo anamunyoza ndipo anati, “Iwe ndiye ophunzira wa
munthuyu! Ife ndife ophunzira a Mose! 29 Ife tikudziwa kuti Mulungu
anayankhula kwa Mose, koma za munthu uyu, ife sitikudziwa ngakhale
kumene akuchokera.”
30 Munthuyo anayankha kuti, “Tsopano izi ndi zodabwitsa! Inu
simukudziwa kumene akuchokera, komabe iye watsekula maso anga.
31 Ife tikudziwa kuti Mulungu samvera wochimwa. Iye amamvera munthu
woopa Mulungu amene amachita chifuniro chake. 32 Palibe amene
anamvapo za kutsekula maso a munthu wobadwa wosaona. 33 Ngati
munthu uyu akanakhala wosachokera kwa Mulungu, palibe chimene Iye
akanachita.”
34 Pamenepo anayankha kuti, “Iwe unabadwa mu uchimo kotheratu;
bwanji ukuyesa kutiphunzitsa ife!” Ndipo anamutulutsa kunja.

### *Kusaona kwa Uzimu*

35 Yesu anamva kuti anamutulutsa kunja ndipo pamene anamupeza
anati, “Kodi ukukhulupirira Mwana wa Munthu?”
36 Munthuyo anafunsa kuti, “Kodi, Ambuye, ameneyo ndi ndani?
Ndiwuzeni kuti ndimukhulupirire Iye?”
37 Yesu anati, “Iwe wamuona tsopano. Zoonadi ndiye amene
akuyankhula nawe.”
38 Pamenepo munthuyo anati, “Ambuye, ndikukhulupirira,” ndipo
anamulambira Iye.
39 Yesu anati, “Ndinabwera pansi pano kudzaweruza kuti osaona aone
ndi openya asaone.”
40 Afarisi ena amene anali pafupi naye anamva akunena izi ndipo
anafunsa kuti, “Chiyani? Kodi ndife osaonanso?”
41 Yesu anati, “Mukanakhala osaona, simukanachimwa; koma tsopano
popeza mukuti mumaona, ndinu ochimwabe.”

## 10

### *M’busa Wabwino ndi Nkhosa Zake*

1 “Zoonadi, Ine ndikukuwuzani inu Afarisi, kuti munthu amene sa-
lowera pa khomo m’khola la nkhosa, koma amalowera pena pake ndi
wakuba ndi wachifwamba. 2 Munthu amene amalowera pa khomo
ndi m’busa wankhosazo. 3 Mlonda amamutsekulira khomo, ndipo
nkhosa zimamvera mawu ake. Iye amaziyitana mayina nkhosa zakezo,
nazitulutsa. 4 Akazitulutsa nkhosa zake zonse, iye amazitsogolera, ndipo
nkhosa zakezo zimamutsata chifukwa zimadziwa mawu ake. 5 Koma
nkhosazo sizidzatsatira mlendo. Izo zidzamuthawa chifukwa sizizindikira
mawu a mlendo.” 6 Yesu ananena mawu ophiphiritsawa, koma Afarisi
sanazindikire zimene ankawawuza.
7 Choncho Yesu anatinso, “Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti Ine ndine
khomo la nkhosa. 8 Onse amene anadza ndisanabwere Ine ndi akuba ndi
achifwamba, ndipo nkhosa sizinawamvere. 9 Ine ndine khomo, aliyense
amene alowa kudzera mwa Ine adzapulumuka. Iye adzalowa ndi kutuluka
ndi kupeza msipu. 10 Mbala sibwera chabe koma kuti idzabe, kupha ndi

kuwononga. Ine ndabwera kuti iwo akhale ndi moyo, ndi kukhala nawo
wochuluka.
11 “Ine ndine M’busa wabwino. M’busa wabwino amataya moyo
wake chifukwa cha nkhosa zake. 12 Wantchito ndi m’busa amene
nkhosazo si zake. Choncho, pamene aona mmbulu ukubwera, iye
amazisiya nkhosazo ndi kuthawa. Ndipo mmbulu umagwira nkhosazo
ndikuzibalalitsa. 13 Munthuyo amathawa chifukwa ndi wantchito ndipo
sasamalira chilichonse cha nkhosazo.
14 “Ine ndine m’busa wabwino. Ine ndimazidziwa nkhosa zanga ndipo
nkhosa zangazo zimandidziwa, 15 monga momwe Atate amandidziwa Ine,
ndiponso Ine kudziwira Atatewo. Ndimapereka moyo wanga chifukwa cha
nkhosa. 16 Ine ndili ndi nkhosa zina zimene sizili za gulu ili. Ine ndiyenera
kuzibweretsanso. Izonso zidzamvera mawu anga, ndipo zidzakhala
gulu limodzi ndi m’busa mmodzi. 17 N’chifukwa chake Atate anga
amandikonda, popeza Ine ndikupereka moyo wanga kuti ndiwutengenso.
18 Palibe amene angawuchotse mwa Ine, koma ndikuwupereka mwaku-
funa kwanga. Ine ndili ndi ulamuliro wa kuwupereka ndi ulamuliro
wakuwutenganso. Lamulo ili ndinalandira kwa Atate anga.”
19 Pa mawu awa Ayuda anagawikananso. 20 Ambiri a iwo anati, “Iye
ndi wogwidwa ndi ziwanda ndi wamisala. Chifukwa chiyani mukumvera
Iye?”
21 Koma ena anati, “Awa si mawu a munthu wogwidwa ndi ziwanda.
Kodi ziwanda zingathe bwanji kutsekula maso a wosaona?”

### *Kusakhulupirira kwa Ayuda*

22 Ku Yerusalemu kunali chikondwerero chokumbukira kupatulidwa
kwa Nyumba ya Mulungu. Inali nthawi yozizira, 23 ndipo Yesu ankayenda
m’bwalo la Nyumbayo ku malo a Solomoni. 24 Ayuda anamuzungulira Iye
akunena kuti, “Kodi iwe udzazunguza malingaliro athu mpaka liti? Ngati
iwe ndi Khristu, tiwuze momveka.”
25 Yesu anayankha kuti, “Ine ndimakuwuzani, koma inu
simukhulupirira. Ntchito zimene ndikuchita m’dzina la Atate anga
zikundichitira umboni, 26 koma inu simukhulupirira chifukwa simuli
a gulu lankhosa zanga. 27 Nkhosa zanga zimamva mawu anga, Ine
ndimazidziwa, ndipo zimanditsata Ine. 28 Ine ndimazipatsa moyo wosatha
ndipo sizidzawonongeka. Palibe amene adzazikwatula m’dzanja langa.
29 Atate anga, amene anandipatsa Ine, ndi akulu kuposa onse. Palibe
amene angazikwatule m’dzanja la Atate anga. 30 Ine ndi Atate ndife
amodzi.”
31 Ayuda anatolanso miyala kuti amugende Iye, 32 koma Yesu
anawawuza kuti, “Ine ndakuonetsani zinthu zambiri zabwino zodabwitsa
kuchokera kwa Atate. N’chifukwa chiti mwa izi chimene mukundigen-
dera?”
33 Ayuda anayankha kuti, “Ife sitikukugenda chifukwa cha izi, koma
popeza ukunyoza Mulungu, chifukwa iwe, munthu wamba, ukuti ndiwe
Mulungu.”
34 Yesu anawayankha kuti, “Kodi sizinalembedwa m’malamulo anu
kuti, ‘Ine ndanena kuti ndinu milungu?’ 35 Ngati anawatcha milungu
anthu amene analandira mawu a Mulungu, pajatu Malemba sangasweke,
36 nanga bwanji uyu amene Atate anamuyika padera monga wake
weniweni ndi kumutuma ku dziko lapansi? Nanga ndi chifukwa chiyani
mukundinena Ine kuti ndikuchita chipongwe? Kodi n’chifukwa choti

ndanena kuti, ‘Ine ndine Mwana wa Mulungu?’ 37 Musandikhulupirire
Ine ngati sindichita ntchito za Atate anga. 38 Koma ngati Ine ndiku-
chita zimenezi, ngakhale kuti simundikhulupirira, khulupirirani ntchito
zodabwitsazo, ndipo mudziwe ndi kuzindikira kuti Atate ali mwa Ine,
ndiponso Ine ndili mwa Atate.” 39 Iwo anafuna kumugwiranso koma
anawapulumuka m’manja mwawo.

40 Kenaka Yesu anabwereranso kutsidya la mtsinje wa Yorodani kumalo
kumene Yohane ankabatiza m’masiku akale. Iye anakhala kumeneko
41 ndipo anthu ambiri anabwera kwa Iye. Iwo anati, “Ngakhale kuti
Yohane sanachite chizindikiro chodabwitsa, zonse zimene Yohane ana-
nena za munthu uyu zinali zoona.” 42 Ndipo pamalo amenewo ambiri
anakhulupirira Yesu.

# 11

### *Imfa ndi Kuukitsidwa kwa Lazaro*

1 Tsopano munthu wina dzina lake Lazaro anadwala. Iye anali wa ku
Betaniya, mudzi wa Mariya ndi mchemwali wake Marita. 2 Mariyayo ndi
yemwe uja amene anadzoza Ambuye ndi mafuta onunkhira napukuta
mapazi ake ndi tsitsi lake. Lazaro wodwalayo anali mlongo wake.
3 Choncho alongo ake anatumiza mawu kwa Yesu kuti, “Ambuye, uja
amene Inu mumamukonda akudwala.”

4 Atamva izi, Yesu anati, “Kudwalako safa nako. Koma akudwala kuti
Mulungu alemekezedwe; ndi kuti Mwana wa Mulungu alemekezedwe
chifukwa cha matendawo.” 5 Yesu anakonda Marita, mchemwali wake
ndi Lazaro. 6 Koma atamva kuti Lazaro akudwala, Iye anakhalabe kumene
anali masiku ena awiri.

7 Kenaka anati kwa ophunzira ake, “Tiyeni tibwerere ku Yudeya.”

8 Ophunzira akewo anati, “Rabi, posachedwa pomwepa Ayuda anafuna
kukugendani ndi miyala, koma Inu mukupitanso komweko?”

9 Yesu anayankha kuti, “Kodi sipali maora khumi ndi awiri pa tsiku?
Munthu amene amayenda masana sapunthwa, popeza akuona chifukwa
cha kuwala kwa dziko lapansi. 10 Koma amene akuyenda usiku amapun-
thwa, chifukwa kuwalako alibe.”

11 Iye atatha kunena izi, anapitirira kuwawuza iwo kuti, “Bwenzi lathu
Lazaro wagona tulo; koma Ine ndikupita kumeneko kukamudzutsa.”

12 Ophunzira ake anayankha kuti, “Ambuye, ngati wagona adzapeza
bwino.” 13 Yesu ankayankhula za imfa yake koma ophunzira ake
ankaganiza kuti amanena za tulo chabe.

14 Ndipo kenaka anawawuza momveka kuti, “Lazaro wamwalira. 15 Ine
ndikukondwera chifukwa cha inu kuti kunalibe kumeneko; koma kuti
mukakhulupirire tiyeni tipiteko.”

16 Pamenepo Tomasi, wotchedwa Didimo, anati kwa ophunzira anzake,
“Tiyeni nafenso tipite, kuti tikafere naye pamodzi.”

### *Yesu Atonthoza Alongo a Lazaro*

17 Yesu atafika, anapeza kuti Lazaro anali atagona m’manda masiku
anayi. 18 Mudzi wa Betaniya unali pafupi ndi Yerusalemu pa mtunda
wosachepera makilomita atatu, 19 ndipo Ayuda ambiri anabwera kwa
Marita ndi Mariya kudzawatonthoza pa imfa ya m’bale wawo. 20 Pamene
Marita anamva kuti Yesu akubwera, anapita kukakumana naye. Koma
Mariya anatsala ku nyumba.

21 Marita anati kwa Yesu, "Ambuye, mukanakhala muli kuno, mlongo
wanga sakanamwalira. 22 Koma ine ndikudziwa kuti ngakhale tsopano
Mulungu adzakupatsani chilichonse chimene mudzamupempha."

23 Yesu anati kwa iye, "Mlongo wako adzauka."

24 Marita anayankha kuti, "Ine ndikudziwa kuti adzauka pa kuukanso
pa tsiku lomaliza."

25 Yesu anati kwa iye, "Ine ndine kuuka ndi moyo. Wokhulupirira Ine,
angakhale amwalira adzakhala ndi moyo. 26 Aliyense amene ali ndi moyo
ndi kukhulupirira Ine sadzamwalira. Kodi iwe ukukhulupirira izi?"

27 Marita anamuwuza Iye kuti, "Inde Ambuye, ine ndikukhulupirira kuti
ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu, amene abwera m'dziko lapansi."

28 Ndipo iye atanena izi anabwerera ndi kukayitana mchemwali wake
Mariya namuyankhula monong'ona pambali, nati, "Aphunzitsi abwera
ndipo akukuyitana." 29 Mariya atamva izi, anayimirira mofulumira napita
kwa Iye. 30 Tsopano n'kuti Yesu asanalowe m'mudzi, koma anali akanali
pa malo pamene Marita anakumana naye. 31 Ayuda amene ankamu-
tonthoza Mariya m'nyumba, anaona mmene iye anayimira mofulumira
ndi kutuluka kunja, iwo anamutsata akuganizira kuti ankapita ku manda
kukalirira kumeneko.

32 Mariya anafika pamalo pamene panali Yesu ndipo atamuona, anagwa
pa mapazi ake ndipo anati, "Ambuye mukanakhala muli kuno mlongo
wanga sakanamwalira."

33 Yesu ataona iye akulira, ndi Ayuda amene anabwera naye akuliranso,
anakhudzidwa kwambiri ndi kuvutika mu mzimu. 34 Iye anafunsa kuti,
"Kodi mwamuyika kuti?"

Iwo anayankha kuti, "Ambuye tiyeni mukaone."

35 Yesu analira.

36 Pamenepo Ayuda anati, "Taonani mmene Iye anamukondera Lazaro!"

37 Koma ena a iwo anati, "Iye amatsekula maso a munthu wosaona, kodi
sakanakhoza kuletsa kuti munthu uyu asamwalire?"

### *Yesu Aukitsa Lazaro*

38 Yesu atakhudzidwanso kwambiri anafika ku manda. Manda akewo
anali phanga ndipo anatsekapo ndi mwala. 39 Yesu anati, "Chotsani
mwala."

Marita mlongo wa womwalirayo anati, "Koma Ambuye, nthawi ino
wayamba kununkha, pakuti wakhala m'menemu masiku anayi."

40 Kenaka Yesu anati, "Kodi Ine sindinakuwuze kuti ngati iwe
ukhulupirira, udzaona ulemerero wa Mulungu?"

41 Choncho iwo anachotsa mwalawo. Kenaka Yesu anayang'ana
kumwamba ndikuti, "Atate, Ine ndikukuthokozani chifukwa mu-
mandimvera. 42 Ine ndimadziwa kuti Inu mumandimvera nthawi zonse,
koma Ine ndanena izi chifukwa cha anthu amene ayima pano, kuti iwo
akhulupirire kuti Inu munanditumi Ine."

43 Yesu atanena izi, Iye anayitana ndi mawu ofuwula kuti, "Lazaro,
tuluka!" 44 Munthu womwalirayo anatuluka, womangidwa miyendo ndi
manja ndi nsalu za ku manda, ndi nkhope yake yokulungidwa nsalu.

Yesu anawawuza kuti, "M'masuleni, ndipo muloleni apite."

### *Ayuda Apangana za Kupha Yesu*

45 Choncho Ayuda ambiri amene anabwera kudzamuchereza Mariya ndi
kuona zimene Yesu anachita anamukhulupirira Iye. 46 Koma ena a iwo

anapita kwa Afarisi ndi kukawawuza zimene Yesu anachita. 47 Kenaka
akulu a ansembe ndi Afarisi anayitanitsa msonkhano wa akulu olamulira.
Iwo anafunsa kuti, “Kodi ife tikuchita chiyani? Pano pali munthu
uyu akuchita zizindikiro zodabwitsa zambiri. 48 Ngati ife timuleka kuti
apitirize chotere, aliyense adzamukhulupirira Iye, ndipo kenaka Aroma
adzabwera ndi kudzatenga malo athu pamodzi ndi dziko lathu.”

49 Kenaka mmodzi wa iwo, dzina lake Kayafa, amene anali mkulu
wa ansembe chaka chimenecho, anayankhula kuti, “Inu simukudziwa
kanthu kalikonse! 50 Inu simukuzindikira kuti kuli bwino kwa inu kuti
munthu mmodzi afe m’malo mwa anthu kusiyana ndi kuti mtundu wonse
uwonongeke.”

51 Iye sananene izi mwa iye yekha, koma monga mkulu wa ansembe
chaka chimenecho ananenera kuti Yesu anayanera kufera mtundu wa
Ayuda, 52 ndipo osati mtundu okhawo komanso kwa ana ena a Mulungu
onse obalalikana, kuti awabweretse pamodzi ndi kuwapanga kukhala
amodzi. 53 Choncho kuyambira tsiku limeneli iwo anakonzekera za kuti
amuphe.

54 Chifukwa cha ichi Yesu sanayendenso moonekera pakati pa Ayuda.
M’malo mwake Iye anapita ku chigawo cha kufupi ndi chipululu, ku mudzi
wa Efereimu, kumene Iye anakhalako ndi ophunzira ake.

55 Nthawi ya Paska wa Ayuda itayandikira, ambiri anakwera kupita ku
Yerusalemu kuchokera ku madera a ku midzi chifukwa cha mwambo wa
kuyeretsedwa Paska asanafike. 56 Iwo anapitiriza kumufunafuna Yesu,
ndipo pamene ankayimirira m’bwalo la Nyumba ya Mulungu anafunsana
wina ndi mnzake kuti, “Kodi ukuganiza chiyani? Kodi Iye sabwera konse
kuphwando?” 57 Koma akulu a ansembe ndi Afarisi anapereka lamulo
kuti ngati wina aliyense adziwe kumene kunali Yesu, iye akawawuze kuti
akamugwire.

# 12

### *Mariya Adzoza Mapazi a Yesu*

1 Masiku asanu ndi limodzi Paska asanafike, Yesu anafika ku Be-
taniya, kumene kumakhala Lazaro, amene Yesu anamuukitsa kwa akufa.
2 Kumeneko anamukonzera Yesu chakudya cha madzulo. Marita ana-
tumikira pamene Lazaro anali mmodzi wa iwo amene anakhala nawo
pa chakudyacho. 3 Kenaka Mariya anatenga botolo la mafuta a nadi,
onunkhira bwino kwambiri, amtengowapatali; Iye anadzoza mapazi a
Yesu napukuta ndi tsitsi lake. Ndipo nyumba yonse inadzaza ndi fungo
lonunkhira bwino la mafutawo.

4 Koma mmodzi wa ophunzira ake, Yudasi Isikarioti, amene pambuyo
pake adzamupereka anati, 5 “N’chifukwa chiyani mafuta awa sanagulit-
sidwe ndipo ndalama zake n’kuzipereka kwa osauka?” Mafutawo anali a
mtengo wa malipiro a chaka chimodzi. 6 Iye sananene izi chifukwa cha
kuganizira osauka koma chifukwa anali mbava; ngati wosunga thumba la
ndalama, amabamo zomwe ankayikamo.

7 Yesu anayankha kuti, “Mulekeni. Mafutawa anayenera kusungidwa
mpaka tsiku loyika maliro anga. 8 Inu mudzakhala ndi osauka nthawi
zonse, koma simudzakhala nane nthawi zonse.”

9 Pa nthawi imeneyi gulu lalikulu la Ayuda linadziwa kuti Yesu anali
kumeneko, ndipo linabwera, sichifukwa cha Iye yekha koma kudzaonanso

Lazaro, amene anamuukitsa kwa akufa. 10 Choncho akulu a ansembe
anakonza njira yoti aphenso Lazaro, 11 pakuti chifukwa cha iye Ayuda
ambiri amapita kwa Yesu ndi kumukhulupirira.

### *Yesu Alowa mu Yerusalemu*

12 Tsiku lotsatira, gulu lalikulu la anthu lomwe linabwera kuphwando
linamva kuti Yesu anali m'njira kupita ku Yerusalemu. 13 Iwo anatenga
nthambi za kanjedza ndi kupita kukakumana naye, akufuwula kuti,
"Hosana!

"Wodala Iye amene akubwera m'dzina la Ambuye!

"Yodala Mfumu ya Israeli!"

14 Yesu anapeza bulu wamng'ono ndi kukwerapo, monga kunalembedwa
kuti:
15 "Usachite mantha mwana wamkazi wa Ziyoni;
taona mfumu yako ikubwera,
itakhala pa mwana wabulu."

16 Poyamba ophunzira ake sanamvetsetse zonsezi. Koma pomwe Yesu
analemekezedwa ndi pamene anazindikira kuti zinthu izi zinalembedwa
ndipo kuti anamuchitira Iye.
17 Tsopano gulu la anthu lomwe linali naye pa nthawi imene amaukit-
sidwa Lazaro ku manda linapitiriza kuchitira umboni. 18 Anthu ambiri,
anapita kukakumana naye, chifukwa iwo anamva kuti Iye anachita
chizindikiro chodabwitsachi. 19 Choncho Afarisi anati kwa wina ndi
mnzake, "Taonani, palibe chimene mwachitapo. Anthu onse akumutsatira
Iye!"

### *Agriki Afuna Kuona Yesu*

20 Tsopano panali Agriki ena pakati pa amene anapita kukapembedza
ku phwando. 21 Iwo anabwera kwa Filipo, wochokera ku Betisaida wa
ku Galileya, ndi pempho, nati, "Akulu, ife tikufuna kuona Yesu." 22 Filipo
anapita kukawuza Andreya; Andreya ndi Filipo pamodzi anakawuza Yesu.
23 Yesu anayankha kuti, "Nthawi yafika yakuti Mwana wa Munthu
alemekezedwe. 24 Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti, 'Mbewu ya tirigu
imakhala imodzi yokha ngati sikugwa m'nthaka ndi kufa. Koma ngati
imfa, imabereka mbewu zambiri.' 25 Munthu amene amakonda moyo
wake adzawutaya, pamene munthu amene amadana ndi moyo wake
m'dziko lino lapansi adzawusungira ku moyo wosatha. 26 Aliyense
amene atumikira Ine ayenera kunditsata; ndipo kumene Ine ndili,
wotumikira wanga adzakhalanso komweko. Atate anga adzalemekeza
amene atumikira Ine.
27 "Moyo wanga ukuvutika tsopano, kodi ndidzanena chiyani? Ndinene
kuti Atate pulumutseni ku nthawi ino? Ayi. Chifukwa chimene Ine
ndinabwera pa nthawi iyi ndi chimenechi. 28 Atate, lemekezani dzina
lanu!"
Kenaka mawu anabwera kuchokera kumwamba, "Ine ndalilemekeza,
ndipo ndidzalilemekezanso." 29 Gulu la anthu lomwe linali pamenepo
litamva linati, "Kwagunda bingu," ena anati, "Mngelo wayankhula kwa
Iye."
30 Yesu anati, "Mawu awa abwera chifukwa cha inu osati chifukwa
cha Ine. 31 Ino tsopano ndi nthawi yachiweruzo pa dziko lapansi;

tsopano olamulira wa dziko lapansi adzathamangitsidwa. 32 Koma Ine,
akadzandipachika pa dziko lapansi, ndidzakokera anthu onse kwa Ine."
33 Iye ananena izi kuti aonetse mmene adzafere.
34 Gulu la anthu linayankha kuti, "Ife tinamva kuchokera m'malamulo
kuti Khristu adzakhala kwamuyaya, nanga bwanji Inu mukunena kuti,
'Mwana wa Munthu ayenera kukwezedwa?' Kodi Mwana wa Munthuyu
ndani?"
35 Kenaka Yesu anawawuza kuti, "Inu mukhala ndi kuwunika kwa
nthawi pang'ono. Yendani pamene mukanali ndi kuwunika, kuti mdima
usakupitirireni. Munthu amene amayenda mu mdima sadziwa kumene
akupita. 36 Khulupirirani kuwunika, pamene mukanali ndi kuwunika, kuti
mukhale ana a kuwunika." Yesu atamaliza kuyankhula izi, Iye anachoka
nabisala kuti asamuone.

### *Ayuda Apitirira Kusakhulupirira*

37 Ngakhale Yesu anachita zizindikiro zodabwitsa zonsezi pamaso pawo,
sanamukhulupirirebe. 38 Izi zinakwaniritsa mawu a mneneri Yesaya kuti:
"Ambuye, wakhulupirira uthenga wathu ndani,
ndipo ndi kwa yani komwe mkono wa Ambuye wavumbulutsidwa?"
39 Pa chifukwa cha ichi iwo sanakhulupirire, chifukwa Yesaya anane-
nanso kuti:
40 "Iye wachititsa khungu maso awo
ndi kuwumitsa mitima yawo,
kotero kuti iwo sangathe kuona ndi maso awo,
kapena kuzindikira ndi mitima yawo,
kapena kutembenuka kuti Ine ndikanawachiza."
41 Yesaya ananena izi chifukwa anaona ulemerero wa Yesu ndi kuyankhula
za Iye.
42 Komabe pa nthawi yomweyi ambiri ngakhale atsogoleri
anakhulupirira Iye. Koma chifukwa cha Afarisi iwo sanavomereze
chikhulupiriro chawo chifukwa amaopa kuti angawatulutse m'sunagoge;
43 pakuti iwo amakonda kuyamikiridwa ndi anthu kuposa kuyamikiridwa
ndi Mulungu.
44 Kenaka Yesu anafuwula nati, "Munthu aliyense amene akhulupirira
Ine, sakhulupirira Ine ndekha, komanso Iye amene ananditumа Ine. 45 Iye
amene waona Ine, waonanso Iye amene ananditumа Ine. 46 Ine ndabwera
m'dziko lapansi monga kuwunika, kotero palibe amene amakhulupirira
Ine n'kumakhalabe mu mdima.
47 "Ndipo munthu amene amva mawu anga koma osawasunga, Ine
sindimuweruza. Pakuti Ine sindinabwere kudzaweruza dziko lapansi,
koma kudzapulumutsa. 48 Iye amene akana Ine ndipo salandira mawu
anga ali ndi womuweruza. Tsiku lomaliza mawu amene ndiyankhulawa
adzamutsutsa. 49 Pakuti Ine sindiyankhula mwa Ine ndekha, koma
Atate amene ananditumа amandilamulira choti ndinene ndi momwe
ndinenere. 50 Ine ndikudziwa kuti lamulo lake ndi moyo wosatha.
Choncho chilichonse chimene Ine ndinena ndi chimene Atate andiwuza."

## 13

### *Yesu Asambitsa Mapazi a Ophunzira Ake*

1 Inali pafupifupi nthawi ya phwando la Paska. Yesu anadziwa
kuti nthawi yafika yoti achoke m'dziko lapansi ndi kupita kwa Atate.

Atawakonda ake amene anali m'dziko lapansi, Iye anawaonetsa chikondi
chake chonse.
2 Atayamba kudya mgonero, mdierekezi anali atalowa kale mu mtima
wa Yudasi Isikarioti mwana wa Simoni, kuti amupereke Yesu. 3 Yesu
podziwa kuti Atate anamupatsa Iye zonse m'manja mwake, ndi kuti
Iye anachokera kwa Mulungu ndipo amabwerera kwa Mulunguyo;
4 anayimirira kuchoka pa chakudya navula zovala zake natenga nsalu
yopukutira nadzimanga m'chiwuno mwake. 5 Atachita izi, anathira
madzi m'beseni ndi kuyamba kusambitsa mapazi a ophunzira ake, ndi
kuwapukuta ndi chopukutira chimene anachimanga m'chiwuno mwake.
6 Atafika pa Petro, Petroyo anati kwa Iye, "Ambuye, kodi mudzandisam-
bitsa mapazi anga?"
7 Yesu anayankha kuti, "Iwe sukuzindikira tsopano chimene ndikuchita,
koma udzazindikira m'tsogolo."
8 Petro anati, "Ayi, Inu simudzandisambitsa konse mapazi anga."
Yesu anayankha kuti, "Ngati Ine sindisambitsa mapazi ako, ulibe gawo
mwa Ine."
9 Simoni Petro anayankha kuti, "Ambuye, osati mapazi okha komanso
manja anga ndi mutu wanga womwe!"
10 Yesu anayankha kuti, "Munthu amene wasamba amangofunika
kusamba mapazi ake okha chifukwa thupi lake lonse ndi loyera. Ndipo inu
ndinu oyera, ngakhale kuti si aliyense mwa inu." 11 Pakuti Iye anadziwa
amene adzamupereka, ndipo n'chifukwa chake anati saliyense wa inu ali
woyera.
12 Iye atamaliza kusambitsa mapazi awo anavala zovala zake ndi
kubwerera pamalo pake. Iye anawafunsa kuti, "Kodi mukuzindikira
zimene ndakuchitirani inu? 13 Inu mumanditcha Ine, 'Mphunzitsi' ndi
'Mbuye,' ndipo mumakhoza mukamatero, pakuti ichi ndi chimene Ine
ndili. 14 Tsono ngati Ine, Mbuye wanu ndi Mphunzitsi wanu, ndasambitsa
mapazi anu, inunso muyenera kusambitsana mapazi anu. 15 Ine ndaku-
patsani chitsanzo kuti muzichita monga Ine ndachitira. 16 Zoonadi, Ine
ndikukuwuzani kuti wantchito saposa mbuye wake, kapena wotumidwa
kuposa amene wamutuma. 17 Ngati inu mudziwa zinthu zimenezi,
mudzakhala odala mukamazichita.

### *Yesu Aneneratu za Kuperekedwa Kwake*

18 "Ine sindikunena za inu nonse. Ine ndikudziwa amene ndi-
nawasankha. Koma izi zikukwaniritsa malemba: 'Iye amene akudya nawo
chakudya changa, ndiye amene anandiwukira.'
19 "Ine ndikukuwuzani tsopano zisanachitike zimenezi, kuti pamene za-
chitika, mudzakhulupirire kuti Ine Ndine. 20 Zoonadi, Ine ndikukuwuzani
kuti aliyense amene alandira amene Ine ndamutuma, alandiranso Ine.
Aliyense amene alandira Ine, alandiranso amene ananditumа."

### *Yesu Aneneratu za Kuperekedwa Kwake*

21 Yesu atanena izi, anavutika kwambiri mu mzimu ndipo anachitira
umboni kuti, "Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti mmodzi mwa inu
adzandipereka."
22 Ophunzira ake anapenyetsetsana wina ndi mnzake, posadziwa kuti
amanena za yani. 23 Mmodzi wa ophunzira ake amene Yesu anamukonda,
anali atatsamira pachifuwa chake. 24 Simoni Petro anamukodola wophun-
zirayo ndi kuti, "Mufunseni akunena za yani."

25 Atamutsamiranso Yesuyo, anamufunsa Iye kuti, “Ambuye, kodi ndani?”
26 Yesu anayankha kuti, “Iye amene ndidzamupatsa buledi amene ndanyema ndikususa ndi ameneyo.” Kenaka, atasunsa gawo la buledi, Iye anapereka kwa Yudasi Isikarioti, mwana wa Simoni. 27 Nthawi yomweyo
Yudasi atangodya bulediyo, Satana analowa mwa Iye.
Yesu anamuwuza Iye kuti, “Chomwe ukufuna kuchita, chita msanga.”
28 Koma panalibe ndi mmodzi yemwe pa chakudyapo amene anamvetsa chifukwa chimene Yesu ananenera izi kwa iye. 29 Popeza Yudasi amasunga
ndalama, ena amaganiza kuti Yesu amamuwuza iye kuti akagule zomwe zimafunika pa phwando, kapena kukapereka kanthu kena kake kwa osauka. 30 Nthawi yomweyo Yudasi atangodya buledi, anatuluka, ndipo
unali usiku.

### *Yesu Aneneratu kuti Petro Adzamukana*

31 Yudasi atatuluka, Yesu anati, “Tsopano Mwana wa Munthu walemekezedwa, ndipo mwa Iyeyu Mulungu walemekezedwanso. 32 Ngati
Mulungu walemekezedwa mwa Iye, Mulungu mwini adzalemekezanso Mwana, ndipo amulemekeza nthawi yomweyo.
33 “Ana anga, Ine ndikhala nanu kwa nthawi yochepa chabe. Inu mudzandifunafuna Ine, ndipo monga momwe ndinawawuzira Ayuda, choncho Ine ndikukuwuzani tsopano kuti, kumene Ine ndikupita, inu simungabwereko.
34 “Lamulo latsopano limene ndikukupatsani ndi lakuti: Kondanani wina ndi mnzake, monga momwe Ine ndinakonda inu. Nanunso mukondane wina ndi mnzake. 35 Mukamakondana aliyense adzadziwa
kuti ndinu ophunzira anga.”
36 Simoni Petro anafunsa kuti, “Ambuye, kodi mukupita kuti?”
Yesu anayankha kuti, “Kumene Ine ndikupita iwe sunganditsatire tsopano, koma udzanditsatira m’tsogolo.”
37 Petro anafunsa kuti, “Ambuye, n’chifukwa chiyani ine sindingakutsatireni tsopano? Ine ndidzapereka moyo wanga chifukwa cha Inu.”
38 Kenaka Yesu anayankha kuti, “Kodi iwe udzalolera kutaya moyo chifukwa cha Ine? Zoonadi, Ine ndikukuwuza kuti tambala asanalire, iwe udzandikana katatu!”

# 14

### *Yesu Atonthoza Ophunzira Ake*

1 “Mtima wanu usavutike. Khulupiririrani Mulungu; khulupiririrani
Inenso. 2 M’nyumba mwa Atate anga muli zipinda zambiri. Kukanakhala kuti mulibemo ndikanakuwuzani. Ine ndikupita kumeneko kukakukonzerani malo. 3 Ndipo ndikapita kukakukonzerani malo, ndidzabweranso
kudzakutengani, kuti kumene kuli Ineko, inunso mukakhale komweko.
4 Inu mukudziwa njira ya kumene Ine ndikupita.”

### *Yesu Njira ya kwa Atate*

5 Tomasi anati kwa Iye, “Ambuye ife sitikudziwa kumene Inu mukupita, nanga tingadziwe bwanji njirayo?”
6 Yesu anayankha kuti, “Ine ndine njira, choonadi ndi moyo. Palibe munthu angafike kwa Atate popanda kudzera mwa Ine.
7 Mukanandidziwadi Ine, mukanadziwanso Atate anga. Kuyambira tsopano, mukuwadziwa ndipo mwawaona.”

8 Filipo anati, “Ambuye, tionetseni Atatewo ndipo ife tikhutitsidwa.”

9 Yesu anayankha kuti, “Kodi iwe Filipo, ndakhala pakati panu nthawi
yonseyi ndipo iwe sukundidziwabe? Aliyense amene waona Ine, wao-
nanso Atate. Tsono ukunena bwanji kuti, ‘Tionetseni Atate?’ 10 Kodi
sukukhulupirira kuti Ine ndili mwa Atate, ndipo Atate ali mwa Ine? Mawu
amene Ine ndiyankhula kwa inu si mawu anga okha koma ndi mawu
Atate wokhala mwa Ine, amene akugwira ntchito yake. 11 Khulupirirani
Ine pamene ndi kuti Ine ndili mwa Atate ndipo Atate ali mwa Ine.
Koma ngati si chomwecho, khulupiriranitu Ine chifukwa cha ntchito
zanga zodabwitsa. 12 Zoonadi, Ine ndikukuwuzani kuti aliyense amene
akhulupirira Ine adzachita zimene Ine ndakhala ndikuchita. Iye adzachita
ngakhale zinthu zazikulu kuposa zimenezi, chifukwa ndikupita kwa Atate.
13 Ndipo Ine ndidzachita chilichonse chimene inu mudzapempha m’dzina
langa kuti Atate alemekezedwe mwa Mwana. 14 Ngati mudzapempha
kanthu kalikonse m’dzina langa, Ine ndidzachita.

### *Lonjezo la Mzimu Woyera*

15 “Ngati mundikonda Ine, sungani malamulo anga. 16 Ine ndidza-
pempha Atate, ndipo adzakupatsani Nkhoswe ina kuti izikhala nanu
nthawi zonse. 17 Nkhosweyo ndiye Mzimu wachoonadi. Dziko lapansi
silingalandire Nkhosweyi chifukwa samuona kapena kumudziwa. Koma
inu mumamudziwa pakuti amakhala nanu ndipo adzakhala mwa inu.
18 Ine sindikusiyani nokha kuti mukhale ana amasiye. Ine ndidzabwer-
anso kwa inu. 19 Patsala nthawi yochepa dziko lapansi silidzandionanso
koma inu mudzandiona. Popeza kuti Ine ndili ndi moyo, inunso
mudzakhala ndi moyo. 20 Tsiku limenelo inu mudzazindikira kuti Ine
ndili mwa Atate, ndipo inu muli mwa Ine, ndipo Ine ndili mwa inu.
21 Iye amene amadziwa malamulo anga ndi kuwasunga ndiye amene
amandikonda. Wokonda Ine adzakondedwa ndi Atate wanga ndipo Inenso
ndidzamukonda ndikudzionetsa ndekha kwa iye.”

22 Kenaka Yudasi (osati Yudasi Isikarioti) anati, “Koma Ambuye,
n’chifukwa chiyani mukufuna kudzionetsa nokha kwa ife, osati ku dziko
lapansi?”

23 Yesu anamuyankha kuti, “Ngati wina aliyense andikonda Ine, adza-
sunga mawu anga. Atate wanga adzamukonda, ndipo Ife tidzabwera ndi
kukhala naye. 24 Iye amene sandikonda Ine sasunga mawu anga. Mawu
awa amene mukumva si anga ndi a Atate amene ananditumа Ine.

25 “Ndayankhula zonsezi ndikanali nanu. 26 Koma Nkhosweyo, Mzimu
Woyera, amene Atate adzamutumiza m’dzina langa adzakuphunzitsani
zinthu zonse, ndipo adzakukumbutsani zonse zimene ndinakuwuzani.
27 Ine ndikukusiyirani mtendere. Ndikukupatsani mtendere wanga.
Ine sindikukupatsani monga dziko lapansi limaperekera. Mtima wanu
usavutike ndipo musachite mantha.

28 “Inu munamva Ine ndikunena kuti, ‘Ine ndikupita ndipo ndidzabw-
eranso kwa inu.’ Mukanandikonda, mukanasangalala kuti Ine ndikupita
kwa Atate, pakuti Atate ndi wamkulu kuposa Ine. 29 Ine ndakuwuzani
tsopano zisanachitike, kuti zikadzachitika mudzakhulupirire. 30 Ine
sindiyankhulanso nanu zambiri nthawi yayitali popeza wolamulira dziko
lapansi akubwera. Iye alibe mphamvu pa Ine, 31 koma kuti dziko lapansi
lizindikire kuti Ine ndimakonda Atate ndi kuti ndimachita zokhazokha
zimene Atate wandilamulira Ine.

"Nyamukani; tizipita."

# 15

### *Mpesa ndi Nthambi*

[1] "Ine ndine mpesa weniweni, ndipo Atate anga ndiye mwini munda.
[2] Iye amadula nthambi iliyonse ya mwa Ine imene sibala chipatso, koma
nthambi iliyonse imene imabala chipatso amayisadzira bwino kuti ibale
zipatso zambiri. [3] Inu ndinu oyera kale chifukwa cha mawu amene
ndayankhula inu. [4] Khalani mwa Ine, monga Ine ndili mwa inu. Palibe
nthambi imene ingabereke chipatso pa yokha ngati sinalumikizike ku
mpesa. Chomwechonso inu simungathe kubereka chipatso pokhapokha
mutakhala mwa Ine.
[5] "Ine ndine mpesa; inu ndinu nthambi zake. Ngati munthu akhala mwa
Ine ndi Ine mwa iye, adzabereka zipatso zambiri; popanda Ine simungathe
kuchita kanthu. [6] Ngati wina aliyense sakhala mwa Ine, iyeyo ali ngati
nthambi imene yatayidwa ndi kufota. Nthambi zotero zimatoledwa,
kuponyedwa pa moto ndi kupsa. [7] Ngati inu mukhala mwa Ine ndipo
mawu anga akhala mwa inu, pemphani chilichonse chimene mukufuna
ndipo mudzapatsidwa. [8] Atate anga amalemekezedwa mukamabereka
zipatso zochuluka, ndipo potero mudzionetsa kuti ndinu ophunzira anga.
[9] "Monga momwe Atate amandikondera Ine, Inenso ndakukondani.
Tsopano khalani m'chikondi changa. [10] Ngati mumvera malamulo anga,
mudzakhala m'chikondi changa, monga Ine ndimamvera malamulo a
Atate anga, ndipo ndimakhala m'chikondi chawo. [11] Ine ndakuwuzani
izi kuti chimwemwe changa chikhale mwa Inu, kuti chimwemwe chanu
chikhale chokwanira. [12] Lamulo langa ndi ili: 'Kondanani wina ndi
mnzake monga Ine ndakonda inu.' [13] Palibe munthu ali ndi chikondi
choposa ichi, choti munthu n'kutaya moyo wake chifukwa cha abwenzi
ake. [14] Inu ndinu abwenzi anga ngati muchita zimene Ine ndikulamu-
lani. [15] Ine sindikutchulaninso antchito, chifukwa wantchito sadziwa
zimene bwana wake akuchita. M'malo mwake Ine ndakutchani abwenzi
pakuti zilizonse zimene ndinaphunzira kwa Atate, Ine ndakudziwitsani.
[16] Inu simunandisankhe Ine, koma Ine ndinakusankhani kuti mupite
ndi kukabereka zipatso, zipatso zake za nthawi yayitali. Choncho
Atate adzakupatsani chilichonse chimene mudzapempha m'dzina langa.
[17] Lamulo langa ndi ili: 'Muzikondana.'

### *Dziko Lapansi Limada Ophunzira a Yesu*

[18] "Ngati dziko lapansi lidana nanu, dziwani kuti linayamba kudana
ndi Ine. [19] Inu mukanakhala anthu a dziko lapansi, dziko lapansi
likanakukondani ngati anthu ake omwe. Koma mmene zilili, inu si
anthu a dziko lapansi. Ine ndakusankhani kuchokera m'dziko lapansi,
n'chifukwa chake dziko lapansi limakudani. [20] Kumbukirani mawu
amene ndinayankhula nanu akuti, 'Palibe wantchito amene amaposa
bwana wake.' Ngati anandizunza Ine, iwo adzakuzunzaninso inu.
Ngati anamvera chiphunzitso changa, iwo adzamvera chanunso. [21] Iwo
adzakuchitani zimenezi chifukwa cha dzina langa, popeza sakudziwa
amene ananditumа Ine. [22] Ine ndikanapanda kubwera ndi kuyankhula
nawo, sakanakhala ndi mlandu. Koma tsopano alibe choti n'kukanira
mlandu wawo. [23] Iye amene amadana ndi Ine amadanansо Atate anga.
[24] Ine ndikanapanda kuchita pakati pawo zinthu zimene wina aliyense

sanachitepo, iwo sakanakhala ochimwa. Koma tsopano aona zodabwitsa
izi, komabe akundida Ine pamodzi ndi Atate anga. 25 Koma zatere kuti
zikwaniritse zimene zinalembedwa m'malamulo awo: 'Iwo anandida Ine
popanda chifukwa.'

*Ntchito ya Mzimu Woyera*

26 "Nkhoswe ikadzabwera imene Ine ndidzakutumizireni kuchokera
kwa Atate, ndiye Mzimu Woyera wachoonadi amene achokera kwa Atate,
Iyeyo adzandichitira umboni Ine. 27 Inunso mudzandichitira umboni Ine,
popeza mwakhala nane kuchokera pachiyambi."

## 16

1 "Ine ndakuwuzani zonsezi kuti musadzakhumudwe. 2 Iwo adzaku-
chotsani m'sunagoge mwawo. Kunena zoona, nthawi ikubwera imene
aliyense amene adzakuphani adzaganiza kuti akutumikira Mulungu.
3 Iwo adzachita zoterozo chifukwa sanadziwe Atate kapena Inenso.
4 Ine ndakuwuzani izi kuti nthawi ikadzafika mudzakumbukire kuti Ine
ndinakuchenjezani kale. Ine sindinakuwuzeni izi poyamba paja chifukwa
ndinali nanu."

*Ntchito ya Mzimu Woyera*

5 "Tsopano Ine ndikupita kwa Iye amene ananditumа koma palibe
wina mwa inu akundifunsa kuti, 'Kodi mukupita kuti?' 6 Muli ndi
chisoni kwambiri chifukwa ndakuwuzani zimene. 7 Komatu ndakuwuzani
zoona. Ine ndikuti kuli bwino kwa inu kuti ndichoke. Ngati sindichoka,
Nkhosweyo sidzabwera kwa inu, koma ngati Ine ndipita, ndidzamutumiza
kwa inu. 8 Iye akabwera, adzatsutsa dziko lapansi za uchimo, zachilung-
amo ndi zachiweruzo. 9 Za uchimo, chifukwa anthu sakhulupirira
Ine. 10 Za chilungamo, chifukwa Ine ndi kupita kwa Atate, kumene
simudzandionanso. 11 Za chiweruzo, chifukwa wolamulira dziko lino
lapansi waweruzidwa tsopano.
12 "Ine ndili ndi zambiri zoti ndiyankhule nanu, koma simungathe
kuzilandira tsopano. 13 Koma pamene Iye, Mzimu wachoonadi, abwera,
adzakutsogolerani m'choonadi chonse. Iye sadzayankhula mwa Iye
yekha, adzayankhula zokhazo zimene wamva ndipo Iye adzakuwuzani
zimene zikubwera. 14 Iye adzalemekeza Ine chifukwa adzatenga za Ine
nadzakudziwitsani. 15 Zonse za Atate ndi zanga. Ichi n'chifukwa chake Ine
ndanena kuti Mzimu Woyera adzatenga kwa Ine zanga kuti muzidziwe."

*Chisoni cha Ophunzira Chisandulika Chimwemwe*

16 Yesu anapitiriza kuyankhula kuti, "Mwa kanthawi kochepa,
simudzandionanso, ndipo patatha nthawi pang'ono mudzandionanso."
17 Ena a ophunzira ake anati kwa wina ndi mnzake, "Kodi Iye
akutanthauza chiyani ponena kuti, 'Mwa kanthawi kochepa, simudzandio-
nanso,' ndi 'ndipo patatha nthawi pang'ono mudzandionanso,' ndiponso
'chifukwa ndikupita kwa Atate?' " 18 Iwo anapitiriza kufunsana kuti, "Kodi
akutanthauza chiyani, 'kanthawi kochepa?' Ife sitikumvetsetsa chimene
Iye akuyankhula."
19 Yesu anadziwa kuti ankafuna kuti amufunse za zimenezi, choncho
anawafunsa kuti, "Kodi mukufunsana wina ndi mnzake chimene Ine
ndimatanthauza pamene ndinati, 'Mwa kanthawi kochepa simudzandio-
nanso,' ndi 'patatha nthawi pang'ono mudzandionanso?' 20 Zoonadi, Ine
ndikukuwuzani kuti inu mudzalira ndi kubuma pomwe dziko lapansi

lidzakhale likukondwera. Inu mudzamva chisoni, koma chisoni chanu
chidzasandulika chimwemwe. 21 Mayi akamabereka mwana amamva
ululu chifukwa nthawi yake yafika; koma mwana wake akabadwa
amayiwala ululu wake chifukwa cha chimwemwe chake chakuti mwana
wabadwa m'dziko lapansi. 22 Chimodzimodzinso ndi inu. Tsopano
ino ndi nthawi yanu yomva chisoni, koma Ine ndidzakuonaninso
ndipo inu mudzasangalala, ndipo palibe amene adzachotsa chimwemwe
chanu. 23 Tsiku limenelo inu simudzandipemphanso kalikonse. Ine
ndikukuwuzani zoona kuti Atate anga adzakupatsani chilichonse chimene
mudzapempha m'dzina langa. 24 Mpaka tsopano simunapemphe kalikonse m'dzina langa. Pemphani ndipo mudzalandira, ndipo chimwemwe chanu chidzakhala chathunthu.

25 "Ngakhale ndakhala ndikuyankhula m'mafanizo, nthawi ikubwera
imene Ine sindidzagwiritsanso ntchito mafanizo otere koma ndidzakuwuzani momveka za Atate anga. 26 Tsiku limenelo inu mudzapempha
m'dzina langa. Ine sindikunena kuti ndidzapempha Atate m'malo mwanu
ayi. 27 Atate mwini anakukondani chifukwa inu mwandikonda Ine
ndipo mwakhulupirira kuti Ine ndinabwera kuchokera kwa Atate. 28 Ine
ndinabwera kuchokera kwa Atate ndi kulowa m'dziko lapansi. Tsopano ndikulisiya dziko lapansi kubwerera kwa Atate."

29 Kenaka ophunzira ake anati, "Tsopano mukuyankhula momveka
bwino ndi mopanda mafanizo. 30 Tsopano ife tikuona kuti Inu mumadziwa zinthu zonse ndi kuti sipafunika wina aliyense kukufunsani. Mwa ichi ife takhulupirira kuti Inu munachokera kwa Mulungu."

31 Yesu anawafunsa kuti, "Kodi tsopano mwakhulupirira?" 32 Koma
nthawi ikubwera ndipo yafika, pamene inu mudzabalalitsidwa, aliyense ku nyumba yake. Inu mudzandisiya ndekhandekha. Koma Ine sindili ndekha, pakuti Atate anga ali nane.

33 "Ine ndakuwuzani izi kuti mwa Ine mukhale nawo mtendere. M'dziko lapansi mudzakhala nawo mavuto. Koma limbikani mtima! Ine ndaligonjetsa dziko lapansi."

# 17

*Yesu Adzipempherera Yekha*

1 Yesu atatha kunena izi, anayang'ana kumwamba ndipo anapemphera:

"Atate, nthawi yafika. Lemekezani Mwana wanu, kuti Mwana wanuyo
akulemekezeni Inu. 2 Pakuti Inu munamupatsa Iye ulamuliro pa anthu
onse kuti apereke moyo wosatha kwa onse amene mwamupatsa. 3 Tsono
moyo wosathawo ndi uwu: Iwo akudziweni Inu, Mulungu yekhayo
woona, ndi Yesu Khristu, amene Inu mwamutuma. 4 Ine ndabweretsa
ulemerero wanu pa dziko pamene ndamaliza ntchito imene munandipatsa kuti ndi igwire. 5 Ndipo tsopano, Atate, ndilemekezeni Ine pamaso panu ndi ulemerero uja umene ndinali nawo kwa Inu dziko lapansi lisanayambe.

*Yesu Apempherera Ophunzira Ake*

6 "Ine ndawadziwitsa za Inu anthu amene munandipatsa m'dziko lapansi. Iwo anali anu. Inu munawapereka kwa Ine ndipo amvera mawu
anu. 7 Tsopano akudziwa kuti zonse zimene munandipatsa n'zochokera
kwa Inu. 8 Pakuti Ine ndiwapatsa mawu amene Inu munandipatsa
ndipo awalandira. Iwo akudziwa ndithu kuti Ine ndinachokera kwa

Inu, ndipo akukhulupirira kuti Inu ndiye amene munanditumа Ine.
9 Ine ndikuwapempherera. Ine sindikupempherera dziko lapansi, koma
anthu amene Inu mwandipatsa, pakuti ndi anu. 10 Zonse zimene Ine
ndili nazo ndi zanu, ndipo zonse zimene Inu muli nazo ndi zanga.
Choncho Ine ndalemekezedwa mwa iwowo. 11 Ine sindikukhalanso
m'dziko lapansi nthawi yayitali, koma iwo akanali m'dziko lapansi. Ine
ndikubwera kwa Inu. Atate Woyera, atetezeni ndi mphamvu za dzina
lanu. Dzina limene munandipatsa Ine, kuti iwo akhale amodzi monga
Ife tili amodzi. 12 Pamene ndinali nawo, ndinawateteza ndi kuwasunga
mosamala m'dzina limene munandipatsa. Palibe ndi mmodzi yemwe
amene anatayika kupatula yekhayo amene anayenera kuwonongeka
kuti malemba akwaniritsidwe.
13 "Tsopano ndikubwera kwa Inu. Ndikunena izi ndikanali m'dziko
lapansi, kuti iwo akhale ndi muyeso wodzaza wachimwemwe changa
m'kati mwawo. 14 Ine ndawapatsa mawu anu ndipo dziko lapansi
likudana nawo, pakuti sali a dziko lapansi monga Ine sindilinso wa
dziko lapansi. 15 Sindikupempha kuti muwachotse m'dziko lapansi
koma kuti muwateteze kwa woyipayo. 16 Iwo si a dziko lapansi, monga
Ine sindilinso wa dziko lapansi. 17 Ayeretseni ndi choonadi chanu.
Mawu anu ndiye choonadi. 18 Monga Inu munanditumа Ine m'dziko
lapansi, Inenso ndikuwatuma m'dziko lapansi. 19 Chifukwa cha iwowa
Ine ndikudziyeretsa, kuti iwo ayeretsedwenso kwenikweni.

### *Yesu Apempherera Okhulupirira Onse*

20 "Ine sindikupempherera iwo okhawa, komanso
amene adzandikhulupirira chifukwa cha uthenga wawo.
21 Ndikuwapempherera kuti onsewa akhale amodzi. Monga Inu Atate
muli mwa Ine ndi Ine mwa Inu, iwonso akhale mwa Ife kuti dziko
lapansi likhulupirire kuti Inu munanditumа Ine. 22 Ine ndawapatsa
ulemerero umene munandipatsa Ine, kuti akhale amodzi monga Ife
tili amodzi. 23 Ine ndikhale mwa iwo ndipo Inu mwa Ine kuti umodzi
wawo ukhale wangwiro. Choncho dziko lapansi lidzadziwa kuti Inu
munanditumа Ine ndipo Inu mwawakonda iwowa monga momwe Inu
munandikondera Ine.
24 "Atate, Ine ndikufuna kuti anthu amene mwandipatsa Ine adzakhale
ndi Ine kumene kuli Ine, ndi kuona ulemerero wanga, ulemerero
umene munandipatsa chifukwa Inu munandikonda dziko lapansi
lisanalengedwe.
25 "Atate wolungama, ngakhale kuti dziko lapansi silikudziwani Inu,
Ine ndimakudziwani, ndipo iwo amadziwa kuti Inu munanditumа Ine.
26 Ine ndawadziwitsa dzina lanu, ndipo ndidzapitiriza kuwadziwitsa
dzina lanulo, kuti chikondi chomwe munandikonda nacho chikhale
mwa iwo, ndipo Ine mwa iwo."

## 18

### *Amugwira Yesu*

1 Yesu atamaliza kupemphera, Iye anachoka ndi ophunzira ake ndi
kuwoloka chigwa cha Kidroni. Kumbali inayo kunali munda wa Olivi,
ndipo Iye ndi ophunzira ake analowamo.
2 Tsopano Yudasi, amene anamupereka amadziwa malowo chifukwa
Yesu ankakumana ndi ophunzira ake kumeneko. 3 Choncho Yudasi

anabwera ku munda, akutsogolera gulu la asilikali ndi akuluakulu ena
ochokera kwa akulu a ansembe ndi Afarisi. Iwo anali atanyamula miyuni,
nyale ndi zida.
4 Yesu, podziwa zonse zimene zimati zichitike kwa Iye, anatuluka ndi
kuwafunsa kuti, "Kodi mukufuna ndani?"
5 Iwo anayankha kuti, "Yesu wa ku Nazareti."
Yesu anati, "Ndine." (Ndipo Yudasi womuperekayo anali atayima nawo
pamenepo). 6 Pamene Yesu anati, "Ndine," iwo anabwerera m'mbuyo ndi
kugwa pansi.
7 Iye anawafunsanso kuti, "Kodi mukumufuna ndani?"
Ndipo iwo anati, "Yesu wa ku Nazareti."
8 Yesu anayankha kuti, "Ine ndakuwuzani kuti Ndine. Ngati inu
mukufuna Ine, asiyeni anthu awa apite." 9 Izi zinachitika kuti mawu
amene Iye anayankhula akwaniritsidwe: "Ine sindinataye ndi mmodzi
yemwe mwa iwo amene mwandipatsa."
10 Kenaka Simoni amene anali ndi lupanga analitulutsa ndi kutema
nalo wantchito wa wamkulu wa ansembe, nadula khutu lake la kudzanja
lamanja. (Dzina la wantchitoyo ndi Makusi).
11 Yesu analamula Petro kuti, "Bwezera lupanga m'chimake! Kodi Ine
ndisamwere chikho chimene Atate andipatsa?"

### *Amutengera Yesu kwa Anasi*

12 Kenaka gulu la asilikali ndi olamulira wawo ndi akuluakulu a Ayuda
anamugwira Yesu. Iwo anamumanga. 13 Poyamba anapita naye kwa
Anasi amene anali mkamwini wa Kayafa, mkulu wa ansembe chaka
chimenecho. 14 Kayafa anali amene analangiza Ayuda kuti kukanakhala
kwabwino ngati munthu mmodzi akanafera anthu.

### *Petro Akana Yesu Koyamba*

15 Simoni Petro ndi ophunzira wina ankamutsatira Yesu chifukwa
ophunzira uyu amadziwika kwa mkulu wa ansembe. Iye analowa ndi Yesu
m'bwalo la mkulu wa ansembe 16 koma Petro anadikira kunja pa khomo.
Ophunzira winayo amene amadziwika kwa mkulu wa ansembe, anatuluka
ndi kuyankhula ndi mtsikana amene anali mlonda wa pa khomo ndi
kumulowetsa Petro.
17 Mtsikanayo anafunsa Petro kuti, "Kodi iwe sindiwe mmodzi wa
ophunzira a Munthu uyu?"
Iye anayankha kuti, "Ayi, sindine."
18 Popeza kunkazizira, anyamata antchito ndi akuluakulu ena ana-
sonkha moto wamakala namawotha atayimirira mozungulira. Petro
nayenso anayimirira pamodzi ndi iwo namawotha nawo motowo.

### *Mkulu wa Ansembe Amufunsa Yesu*

19 Pa nthawi imeneyi, mkulu wa ansembe anamufunsa Yesu za ophun-
zira ake ndi chiphunzitso chake.
20 Yesu anayankha kuti, "Ine ndinayankhula poyera ku dziko lapansi.
Nthawi zonse ndimaphunzitsa m'sunagoge kapena m'Nyumba ya Mu-
lungu kumene Ayuda onse amasonkhana pamodzi. Ine sindimanena
kanthu mseri. 21 N'chifukwa chiyani mukundifunsa Ine? Afunseni amene
amamva. Zoonadi akudziwa zimene Ine ndinanena."
22 Yesu atanena izi, mmodzi wa akuluakulu amene anali pafupi
anamumenya kumaso. Iye anafunsa kuti, "Mayankhidwe awa ndi woti
ndi kuyankha mkulu wa ansembe?"

23 Yesu anayankha kuti, "Ngati Ine ndanena kanthu kolakwika,
chitirani umboni chimene ndalakwa. Koma ngati ndanena zoona,
n'chifukwa chiyani mwandimenya?" 24 Kenaka Anasi anamutumiza Iye,
ali womangidwabe, kwa Kayafa, mkulu wa ansembe.

### *Petro Akana Yesu Kachiwiri ndi Kachitatu*

25 Pamene Simoni Petro anali chiyimirire kuwotha moto, anafunsidwa
kuti, "Kodi iwe si mmodzi wa ophunzira ake?"

Iye anayankha kuti, "Ayi, sindine."

26 Mmodzi wa antchito a mkulu wa ansembe, m'bale wa munthu amene
anadulidwa khutu ndi Petro anamutsutsa iye kuti, "Kodi sindinakuone iwe
pamodzi ndi Iye m'munda muja?" 27 Petro anakananso, ndipo pa nthawi
yomweyo tambala analira.

### *Yesu ku Bwalo la Pilato*

28 Kenaka Ayuda anamutenga Yesu kuchoka kwa Kayafa ndi kupita ku
nyumba yaufumu ya bwanamkubwa wa Chiroma. Tsopano kunali mmawa, ndipo polewa kudetsedwa monga mwa mwambo Ayuda sanalowe
m'nyumba yaufumuyo; iwo anafuna kuti adye Paska. 29 Choncho Pilato
anatuluka napita kwa iwo ndipo anati, "Kodi ndi milandu yanji imene
mukumuzenga munthu uyu?"

30 Iwo anayankha kuti, "Ngati Iye akanakhala kuti si wolakwa, ife
sitikanamupereka kwa inu."

31 Pilato anati, "Mutengeni inu eni ake ndi kumuweruza Iye monga mwa
malamulo anu."

Ayuda anatsutsa nati, "Koma tilibe ulamuliro wakupha aliyense." 32 Izi
zinachitika kuti mawu a Yesu amene anayankhula kusonyeza mtundu wa
imfa imene Iye anati adzafe nayo akwaniritsidwe.

33 Kenaka Pilato anapita m'kati mwa nyumba yaufumu nayitanitsa Yesu,
ndipo anamufunsa kuti, "Kodi iwe ndi mfumu ya Ayuda?"

34 Yesu anafunsa kuti, "Kodi amenewo ndi maganizo anu wokha?
Kapena kuti ena anakuwuzani za Ine?"

35 Pilato anayankha kuti, "Kodi iwe ukuganiza kuti ine ndine Myuda?
Ndi anthu ako ndi akulu a ansembe ako amene akupereka iwe kwa ine.
Kodi walakwanji?"

36 Yesu anati, "Ufumu wanga si wa dziko lapansi lino. Ukanakhala
wa pansi pano, antchito anga akanachita nkhondo kulepheretsa Ayuda
kundigwira. Koma tsopano ufumu wanga ndi wochokera kumalo ena."

37 Pilato anati, "Kani ndiwe mfumu!"

Yesu anayankha kuti, "Inu mwalondola ponena kuti, Ine ndine mfumu. Kunena zoona, Ine ndinabadwa chifukwa cha chimenechi, ndipo n'chifukwa chake ndinabwera m'dziko lapansi, kudzachitira umboni choonadi. Aliyense amene ali mbali yachoonadi amamvera mawu anga."

38 Pilato anafunsa kuti, "Kodi choonadi n'chiyani?" Ndi mawu awa
iye anapitanso kwa Ayuda ndipo anati, "Ine sindikupeza mlandu mwa
Iye. 39 Koma ndi mwambo wanu kuti pa nthawi ya Paska, ine ndikumasulireni wam'ndende mmodzi. Kodi mufuna ndikumasulireni 'Mfumu ya
Ayuda?' "

40 Iwo anafuwula nati, "Ameneyu ayi! Mutipatse ife Baraba!" Barabayo
anali wachifwamba.

# 19

*Yesu Aweruzidwa kuti Aphedwe*

1 Kenaka Pilato anatenga Yesu namukwapula mwankhanza. 2 Asilikali
analuka nkhata yaminga ndi kumuveka pamutu pake. Kenaka anamu-
veka mkanjo wapepo 3 ndipo ankapita kwa Iye mobwerezabwereza ndi
kumanena kuti, "Moni mfumu ya Ayuda?" Ndipo amamumenya makofi.
4 Pilato anatulukanso ndipo anati kwa Ayuda, "Taonani, ine ndikumub-
weretsa kuti inu mudziwe kuti ine sindikupeza chifukwa chomuyimbira
mlandu." 5 Pamenepo Yesu anatuluka atavala nkhata yaminga ndi mkanjo
wapepo ndipo Pilato anawawuza kuti, "Nayu munthu uja!"
6 Atangomuona Iye akulu a ansembe ndi akuluakulu ena anafuwula kuti,
"Mpachikeni! Mpachikeni!"

Koma Pilato anayankha kuti, "Inu mutengeni ndi kumupachika. Koma ine sindikupeza chifukwa chomuyimbira mlandu."

7 Ayuda anayimirira nati, "Ife tili ndi lamulo, ndipo molingana ndi
lamulolo, Iyeyu ayenera kuphedwa chifukwa akudzitcha kuti ndi Mwana
wa Mulungu."
8 Pilato atamva zimenezi, anachita mantha kwambiri, 9 ndipo anab-
wereranso m'nyumba yaufumu. Iye anafunsa Yesu kuti, "Kodi uma-
chokera kuti?" Koma Yesu sanayankhe. 10 Pilato anati, "Kodi ukukana
kundiyankhula ine? Kodi sukuzindikira kuti ine ndili ndi mphamvu
yokumasula ndiponso mphamvu yokupachika?"
11 Yesu anayankha kuti, "Inu simukanakhala ndi mphamvu pa
Ine akanapanda kukupatsani kumwamba. N'chifukwa chake amene
wandipereka Ine kwa inu ndiye wochimwa kwambiri."
12 Kuyambira pamenepo Pilato anayesa kuti amumasule Yesu, koma
Ayuda anapitirira kufuwula kuti, "Ngati mumumasula munthuyu kuti
apite, inu si bwenzi la Kaisara."
13 Pilato atamva zimenezi, iye anamutulutsa Yesu kunja ndi kukhala
pansi pa mpando wa woweruza pamalo otchedwa Mwala Wowaka (umene
pa Chiaramaiki ndi Gabata). 14 Linali tsiku lokonzekera Sabata la Paska
ndipo nthawi inali ora lachisanu ndi chimodzi masana.

Pilato anati kwa Ayuda, "Nayi mfumu yanu."

15 Koma iwo anafuwula kuti, "Choka nayeni! Choka nayeni!
Mpachikeni!"

Pilato anafunsa kuti, "Kodi ine ndipachike mfumu yanuyi?"

Akulu a ansembe anayankha kuti, "Ife tilibe mfumu ina koma Kaisara."

16 Pomaliza Pilato anamupereka kwa iwo kuti akapachikidwe. Choncho
asilikali anamutenga Yesu.

*Kupachikidwa kwa Yesu*

17 Atanyamula mtanda wake, anapita kumalo otchedwa "Malo a Bade"
(m'Chiaramaiki amatchedwa Gologota). 18 Pamenepo iwo anamupachika
Iye pamodzi ndi anthu ena awiri, mmodzi mbali ina ndi wina mbali inanso
ndipo Yesu pakati.
19 Pilato analemba chikwangwani chomwe anachikhoma pa mtandapo.
Panalembedwa mawu akuti, YESU WA KU NAZARETI, MFUMU YA AYUDA.
20 Ayuda ambiri anawerenga chikwangwanichi, pakuti pamalo pamene
Yesu anapachikidwapo panali pafupi ndi mzinda ndipo chikwangwanicho
chinalembedwa mu Chiaramaiki, Chilatini ndi Chigriki. 21 Kenaka mkulu
wa ansembe wa Ayuda anakadandaula kwa Pilato nati, "Musalembe kuti

'Mfumu ya Ayuda,' koma kuti munthuyu amadzitcha kuti ndi mfumu ya
Ayuda."
22 Pilato anayankha kuti, "Chimene ine ndalemba, ndalemba."
23 Asilikali atamupachika Yesu, anatenga zovala zake ndi kuzigawa
zigawo zinayi, gawo limodzi la aliyense wa iwo, ndi kutsala mwinjiro
wam'kati wokha. Chovala ichi chinawombedwa kuyambira pamwamba
mpaka pansi wopanda msoko.
24 Iwo anati kwa wina ndi mnzake, "Tiyeni tisaching'ambe koma tichite
maere kuti tione amene achitenge."
Izi zinachitika kuti malemba akwaniritsidwe amene anati,
"Iwo anagawana zovala zanga pakati pawo
ndi kuchita maere pa zovala zangazo."
Choncho izi ndi zimene asilikali anachita.
25 Pafupi ndi mtanda wa Yesu panayima amayi ake, mng'ono wa amayi
ake, Mariya mkazi wa Kaliyopa ndi Mariya wa ku Magadala. 26 Yesu
ataona amayi ake pamenepo ndi wophunzira amene Iye anamukonda
atayima pafupipo, Iye anati kwa amayi ake, "Amayi nayu mwana wanu."
27 Anawuzanso wophunzirayo kuti, "Nawa amayi ako." Kuyambira nthawi
imeneyo, wophunzirayo anatenga amayiwo kupita nawo kwawo.

### *Imfa ya Yesu*

28 Atadziwa kuti zonse zatha tsopano komanso kuti malemba akwanir-
itsidwe, Yesu anati, "Ine ndili ndi ludzu." 29 Pomwepo panali mtsuko
wodzaza ndi vinyo wosasa, choncho iwo ananyika chinkhupule ndi
kuchisomeka ku mtengo wa hisope nachifikitsa kukamwa kwa Yesu.
30 Yesu atalandira chakumwachi anati, "Kwatha." Ndipo Iye anaweramitsa
mutu wake napereka mzimu wake.
31 Popeza linali Tsiku Lokonzekera ndipo tsiku linalo linali Sabata
lapadera; Ayuda sanafune kuti mitembo ikhale pa mtanda pa Sabata,
iwo anapempha Pilato kuti akathyole miyendo ndi kutsitsa mitemboyo.
32 Chifukwa chake asilikali anabwera ndi kuthyola miyendo ya munthu
oyamba amene anapachikidwa ndi Yesu ndipo kenaka ya winayo. 33 Koma
atafika pa Yesu ndi kupeza kuti anali atamwalira kale, iwo sanathyole
miyendo yake. 34 M'malo mwake, mmodzi wa asilikaliwo anamubaya
Yesu ndi mkondo m'nthiti, ndipo nthawi yomweyo munatuluka magazi
ndi madzi. 35 Munthu amene anaona izi wapereka umboni ndipo umboni
wake ndi woona. Iye akudziwa kuti akunena choonadi kuti inunso
mukhulupirire. 36 Zinthu izi zinachitika kuti malemba akwaniritsidwe:
"Palibe limodzi la mafupa limene lidzathyoledwa," 37 ndi monga lemba
linanso linena, "Iwo adzayang'ana Iye amene iwo anamubaya."

### *Yesu Ayikidwa M'manda*

38 Kenaka, Yosefe wa ku Arimateyu anakapempha mtembo wa Yesu kwa
Pilato. Tsono Yosefe anali wophunzira wa Yesu koma mobisa chifukwa
iye ankaopa Ayuda. Atalandira chilolezo kwa Pilato, anakatsitsa mtembo
wa Yesu. 39 Nekodimo, munthu amene poyamba pake anabwera kwa
Yesu usiku, anatenga mafuta osakaniza ndi mure ndi aloe wolemera
pafupifupi makilogalamu 32. 40 Pamenepo anatenga mtembo wa Yesu
nawukulunga pamodzi ndi zonunkhiritsa mu nsalu za mtundu woy-
era monga mwa mwambo wa maliro wa Ayuda. 41 Pamalo pamene
anapachikidwa Yesu panali munda ndipo m'mundamo munali manda
atsopano m'mene munali simunayikidwemo aliyense. 42 Chifukwa linali

Tsiku la Ayuda Lokonzekera ndi kuti mandawo anali pafupipo, iwo anayika Yesu m'menemo.

# 20

### *Yesu Auka kwa Akufa*

1 Mmamawa tsiku loyamba la sabata, kukanali kamdimabe, Mariya
wa ku Magadala anapita ku manda ndipo anaona kuti mwala unali
utachotsedwa pa khomo la manda. 2 Choncho anabwerera akuthamanga
kwa Simoni Petro ndi wophunzira winayo, amene Yesu anamukonda,
ndipo anati, "Iwo amuchotsa Ambuye m'manda, ndipo ife sitikudziwa
kumene iwo amuyika Iye!"
3 Choncho Petro ndi wophunzira winayo ananyamuka kupita ku
manda. 4 Onse awiri anathamanga pamodzi koma wophunzira winayo
anamupitirira Petro, nafika ku manda moyambirira. 5 Ndipo mmene
anawerama nasuzumira m'kati mwa manda anaona nsalu zili potero
koma sanalowemo. 6 Kenaka Simoni Petro, amene anali pambuyo
pake, anafika ndi kulowa m'manda. Iye anaona nsaluzo zili pamenepo,
7 pamodzinso ndi nsalu imene anakulungira nayo mutu wa Yesu. Nsaluyi
inali yopindidwa pa yokha yosiyanitsidwa ndi inayo. 8 Pomaliza wophun-
zira winayo, amene anafika ku manda moyambirira, analowanso m'kati,
iye anaona ndi kukhulupirira. 9 (Iwo sanazindikire kuchokera m'malemba
kuti Yesu anayanera kuuka kuchokera kwa akufa).

### *Yesu Aonekera kwa Mariya wa ku Magadala*

10 Kenaka ophunzira anabwerera ku nyumba zawo, 11 koma Mariya
anayima kunja kwa manda akulira. Pamene akulira, anawerama ndi
kusuzumira m'manda 12 ndipo anaona angelo awiri atavala zoyera,
atakhala pamene panali mtembo wa Yesu, mmodzi kumutu ndi wina
kumapazi.
13 Iwo anamufunsa iye kuti, "Amayi, n'chifukwa chiyani mukulira?"
Iye anati, "Amuchotsa Mbuye wanga, ndipo ine sindikudziwa kumene
iwo amuyika." 14 Atanena izi, iye anatembenuka ndipo anaona Yesu
atayima potero koma iye sanazindikire kuti anali Yesu.
15 Iye anati, "Amayi, mukulira chifukwa chiyani? Ndani amene
mukumufunafuna?"
Poganiza kuti anali mwini munda, iye anati, "Bwana, ngati inu mwamu-
chotsa, ndiwuzeni kumene mwamuyika, ndipo ine ndikamutenga."
16 Yesu anati kwa iye, "Mariya."
Anatembenukira kwa Iye nafuwula mu Chiaramaiki kuti, "Raboni!"
(kutanthauza Mphunzitsi).
17 Yesu anati, "Usandigwire Ine, pakuti sindinapite kwa Atate. M'malo
mwake pita kwa abale anga ndikukawawuza kuti, ndikupita kwa Atate
ndi kwa Atate anunso, kwa Mulungu wanga ndi Mulungu wanunso."
18 Mariya wa ku Magadala anapita kwa ophunzira ndi uthenga wakuti,
"Ndamuona Ambuye!" Iye anawawuza iwo kuti Yesu ananena zinthu izi
kwa iye.

### *Yesu Aonekera kwa Ophunzira ake Tomasi Palibe*

19 Madzulo a tsiku limenelo limene linali loyamba la Sabata ophunzira
ake ali pamodzi, atatseka ndi kukhoma zitseko chifukwa choopa Ayuda,
Yesu anabwera ndi kuyima pakati pawo nati, "Mtendere ukhale nanu!"

20 Iye atatha kunena izi, anawaonetsa manja ake ndi m'nthiti mwake. Ophunzira anasangalala kwambiri pamene anaona Ambuye.

21 Yesu anatinso, "Mtendere ukhale nanu! Monga Atate ananditumira Ine, Inenso ndikukutumani."
22 Ndi mawu amenewo Iye anawapumira ndipo anati, "Landirani Mzimu Woyera.
23 Ngati mukhululukira aliyense machimo ake, iwo akhululukidwa; ngati simuwakhululukira, iwo sanakhululukidwe."

*Yesu Aonekera kwa Tomasi*

24 Koma Tomasi (otchedwa Didimo), mmodzi wa khumi ndi awiriwo, sanali ndi ophunzira pamene Yesu anabwera.
25 Ophunzira enawo atamuwuza Tomasi kuti iwo anaona Ambuye, iye ananenetsa kuti, "Pokhapokha nditaona zizindikiro za misomali m'manja ake ndi kuyikamo chala changa m'mene munali misomali ndi kukhudza dzanja langa m'nthiti mwake, ine sindidzakhulupirira."

26 Patapita sabata, ophunzira ake analinso m'nyumbamo ndipo Tomasi anali nawo. Ngakhale makomo anali otsekedwa, Yesu anabwera nayima pakati pawo, ndipo anati, "Mtendere ukhale nanu!"
27 Kenaka anati kwa Tomasi, "Ika chala chako apa; ona manja anga. Tambasula dzanja lako ndi kukhudza m'nthiti mwanga. Leka kukayika, khulupirira."

28 Tomasi anati kwa Iye, "Ambuye wanga ndi Mulungu wanga!"

29 Kenaka Yesu anamuwuza kuti, "Kodi wakhulupirira chifukwa wandiona Ine? Ndi odala amene amakhulupirira ngakhale asanaone."

*Cholinga cha Uthenga Wabwino wa Yohane*

30 Yesu anachita zodabwitsa zambiri pamaso pa ophunzira ake zimene sizinalembedwe m'buku lino.
31 Koma izi zalembedwa kuti mukhulupirire kuti Yesu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu, ndi kuti mukakhulupirira mukhale nawo moyo m'dzina lake.

# 21

*Yesu Aonekera kwa Ophunzira ku Nyanja ya Tiberiya*

1 Zitatha izi Yesu anaonekeranso kwa ophunzira ake, m'mbali mwa nyanja ya Tiberiya. Anadzionetsera motere:
2 Simoni Petro, Tomasi (otchedwa Didimo), Natanieli wochokera ku Kana wa ku Galileya, ana a Zebedayo, ndi ophunzira ena awiri anali limodzi.
3 Simoni Petro anawawuza iwo kuti, "Ine ndikupita kukasodza," ndipo iwo anati, "ife tipita nawe." Choncho anapita ndi kulowa m'bwato, koma usiku umenewo sanagwire kanthu.

4 Mmamawa, Yesu anayimirira m'mbali mwa nyanja, koma ophunzira ake sanazindikire kuti anali Yesu.

5 Yesu anawafunsa iwo kuti, "Anzanga, kodi muli nsomba?"

Iwo anayankha kuti, "Ayi."

6 Iye anati, "Ponyani khoka lanu kudzanja lamanja la bwato lanu ndipo mupha kanthu." Atatero, iwo analephera kukoka ukonde chifukwa chakuchuluka kwa nsomba.

7 Kenaka ophunzira amene Yesu amamukonda anati kwa Petro, "Ndi Ambuye!" Petro atangomva iye akunena kuti ndi Ambuye, iye anavala chovala chake (pakuti anali atavula) ndipo analumphira m'nyanja.
8 Ophunzira enawo analowa m'bwato akukoka ukonde odzaza ndi nsomba, popeza iwo sanali kutali kuchokera ku mtunda, pafupifupi

mamita makumi asanu ndi anayi. 9 Atafika pa mtunda, iwo anaona moto
wamakala pamenepo ndi nsomba, ndi buledi.
10 Yesu anawawuza kuti, “Tabweretsa nsomba zina mwagwirazo.”
11 Simoni Petro anakwera m’bwato ndi kukokera khoka ku gombe,
lodzaza ndi nsomba zikuluzikulu 153, komabe ndi nsomba zochuluka
chotero khoka silinang’ambike. 12 Yesu anawawuza kuti, “Bwerani
mudzalandire chakudya chammawa.” Palibe mmodzi wa ophunzira
anayesa kumufunsa Iye, “Kodi ndinu ndani?” Iwo anadziwa kuti anali
Ambuye. 13 Yesu anabwera, natenga buledi ndikuwapatsa iwo, ndipo
anachita chimodzimodzi ndi nsomba. 14 Aka kanali tsopano kachitatu Yesu
akuonekera kwa ophunzira ake Iye ataukitsidwa kwa akufa.

### *Yesu Abwezeretsa Petro*

15 Iwo atamaliza kudya chakudya chammawa, Yesu anati kwa Simoni
Petro, “Simoni, mwana wa Yohane, kodi umandikonda Ine kuposa mmene
amandikondera awa?”
Iye anati, “Inde Ambuye, Inu mukudziwa kuti Ine ndimakukondani.”
Yesu anati, “Samala ana ankhosa anga.”
16 Yesu anatinso, “Simoni, mwana wa Yohane, kodi umandikondadi Ine?”
Iye anayankha kuti, “Inde, Ambuye, Inu mukudziwa kuti ine ndimakukondani.”
Yesu anati, “Weta nkhosa zanga.”
17 Yesu anati kwa iye kachitatu, “Simoni, mwana wa Yohane, kodi
umandikondadi Ine?”
Petro anadzimvera chisoni chifukwa Yesu anamufunsa kachitatu kuti,
“Kodi umandikonda Ine?” Iye anati, “Ambuye, Inu mudziwa zinthu zonse.
Inu mukudziwa kuti Ine ndimakukondani.”
Yesu anati, “Dyetsa nkhosa zanga. 18 Zoonadi, Ine ndikukuwuza
kuti uli wamng’ono unkadziveka wekha lamba ndi kupita kumene
unkafuna; koma ukadzakalamba udzatambasula manja ako ndipo wina
wake adzakuveka ndikukutsogolera kupita kumene sukufuna kupita.”
19 Yesu ananena izi kumuzindikiritsa mtundu wa imfa imene Petro
adzalemekezera nayo Mulungu. Kenaka Iye anati kwa Petro, “Nditsate
Ine!”
20 Petro anatembenuka ndi kuona kuti ophunzira amene Yesu amamukonda
amawatsatira iwo. (Uyu ndi amene anatsamira pachifuwa
cha Yesu pa chakudya chamadzulo ndipo iye anati, “Ambuye, kodi ndi
ndani amene adzakuperekani Inu?” 21 Petro atamuona iye, anafunsa kuti,
“Ambuye, nanga uyu?”
22 Yesu anayankha kuti, “Ine nditafuna kuti akhalebe ndi moyo mpaka
nditabweranso, zikukukhudza bwanji zimenezo? Iwe uyenera kunditsata
Ine.” 23 Chifukwa cha ichi mbiri inafala pakati pa abale kuti wophunzira
uyu sadzafa. Koma Yesu sananene kuti iye sadzafa. Iye anati, “Ine
nditafuna kuti akhalebe ndi moyo mpaka nditabweranso, zikukukhudza
bwanji zimenezo?”
24 Uyu ndi wophunzira amene akuchitira umboni ndipo ndi amene
analemba. Ife tidziwa kuti umboni wake ndi woona.
25 Koma palinso zina zambiri zimene Yesu anachita. Zikanalembedwa
zonsezi, ndikhulupirira dziko lonse lapansi likanasowa malo osungirako
mabuku onse amene akanalembedwa.

# MACHITIDWE A ATUMWI

### *Lonjezo la Mzimu Woyera*

1 M'buku langa loyamba, ndinakulembera iwe Teofilo zonse zimene Yesu
anayamba kuchita ndi kuphunzitsa, 2 mpaka tsiku limene anatengedwa
kupita kumwamba, mwamphamvu ya Mzimu Woyera, atawalangiza
atumwi amene anawasankha. 3 Zitatha zowawa zake Yesu anadzionetsa
kwa ophunzira ake, ndi kuonetsanso maumboni ambiri kuti anali
wamoyo. Iye anadzionetsera kwa iwo ndi kuwaphunzitsa za ufumu
wa Mulungu pa masiku makumi anayi. 4 Nthawi ina atasonkhana
nawo pamodzi, Yesu analamulira ophunzira ake kuti, "Musachoke mu
Yerusalemu, koma mudikire mphatso imene Atate anga analonjeza
yomwe ndinakuwuzani. 5 Pakuti Yohane anakubatizani ndi madzi, koma
posachedwapa inu mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera."

### *Yesu Akwera Kumwamba*

6 Atumwi atasonkhana pamodzi, iwo anamufunsa Iye kuti, "Ambuye,
kodi nthawi ino mubwezeretsa ufumu kwa Israeli?"

7 Yesu anawawuza kuti, "Sikofunika kuti mudziwe za nthawi kapena
masiku amene Atate ayika mwa ulamuliro wawo. 8 Koma mudzalandira
mphamvu Mzimu Woyera akadzafika pa inu; ndipo mudzakhala mboni
zanga mu Yerusalemu, ku Yudeya konse ndi ku Samariya, mpaka ku
malekezero a dziko lapansi."

9 Atatha kuyankhula zimenezi, Yesu anatengedwa kupita kumwamba
ophunzira ake akuona, ndipo anabisika m'mitambo.

10 Yesu akukwera kumwamba, ophunzira ake anayang'anitsitsa ndi
chidwi m'mitambo. Mwadzidzidzi anaona anthu awiri ovala zoyera
atayimirira pambali pawo. 11 Iwo anati, "Inu, anthu a ku Galileya,
chifukwa chiyani mukuyima ndi kumayang'ana m'mitambo? Yesu amene
wachotsedwa pakati panu ndi kupita kumwamba, adzabweranso m'njira
yomweyi mwamuona akupita kumwamba."

### *Matiyasi Alowa M'malo mwa Yudasi Isikarioti*

12 Pamenepo atumwi anabwerera ku Yerusalemu kuchokera ku phiri la
Olivi, mtunda wosakwana kilomita kuchokera mu mzindamo. 13 Atafika
mu mzindamo, analowa m'chipinda chammwamba kumene amakhala.
Amene analipo anali awa: Petro, Yohane, Yakobo ndi Andreya; Filipo ndi
Tomasi, Bartumeyu ndi Mateyu; Yakobo mwana wa Alifeyo ndi Simoni
Zelote ndi Yuda mwana wa Yakobo. 14 Onsewa ndi mtima umodzi
anapitiriza kupemphera pamodzi ndi amayi, ndi Mariya amayi ake a Yesu,
ndiponso abale ake a Yesu.

15 Pa nthawi imeneyo Petro anayimirira pakati pa okhulupirira (gulu
la anthu pafupifupi 120). 16 Iye anati, "Abale anga, Malemba anayenera
kukwaniritsidwa omwe Mzimu Woyera anayankhula kalekale kudzera
mwa Davide za Yudasi, amene anatsogolera amene anamugwira Yesu.
17 Iye anali mmodzi wa gulu lathu ndipo anatumikira pamodzi ndi ife."

18 (Yudasi anagula munda ndi ndalama zimene anazipeza pochita zoyipa
zija; kumeneko, iye anagwa chamutu, naphulika pakati ndipo matumbo
ake wonse anakhuthuka. 19 Aliyense mu Yerusalemu anamva zimenezi,

kotero anatcha mundawo m'chiyankhulo chawo kuti Akeledama, kutan-
thauza, Munda wa Magazi).
[20] Petro anati, "Pakuti kwalembedwa m'buku la Masalimo kuti,
"Nyumba yake isanduke bwinja,
ndipo pasakhale wogonamo.
Ndiponso,
"Wina atenge ntchito yake yautsogoleri.
[21] Chifukwa chake ndi kofunika kusankha mmodzi wa anthu amene akhala
nafe nthawi yonse imene Ambuye Yesu ankayenda nafe, [22] kuyambira pa
nthawi ya ubatizo wa Yohane mpaka nthawi imene Yesu anatengedwa
pakati pathu. Pakuti mmodzi wa anthu awa ayenera kukhala mboni
pamodzi ndi ife zakuuka kwake."
[23] Pamenepo anasankha anthu awiri, Yosefe wotchedwa Barsaba (wodzi-
wikanso kuti Yusto) ndi Matiyasi. [24] Kenaka iwo anapemphera nati, "Am-
buye mukudziwa mtima wa aliyense. Tionetseni amene mwamusankha
mwa awiri awa [25] kuti atenge ntchito iyi ya utumwi, imene Yudasi anasiya
napita kumalo womuyenera." [26] Tsono anachita maere, ndipo maerewo
anagwera Matiyasi. Tsono iye anawonjezedwa pa gulu la atumwi khumi
ndi mmodziwo.

# 2

*Kubwera kwa Mzimu Woyera*

[1] Litafika tsiku la chikondwerero cha Pentekosite, onse anali pamodzi.
[2] Mwadzidzidzi kunamveka mkokomo kuchokera kumwamba ngati wa
mphepo yamphamvu, ndipo inadzaza nyumba yonse imene amakhala.
[3] Iwo anaona zinthu zokhala ngati malilime amoto ogawikana ndipo
anakhala pa aliyense wa iwo. [4] Ndipo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woy-
era, nayamba kuyankhula mu ziyankhulo zina, monga Mzimu Woyerayo
anawayankhulitsa.
[5] Ayuda woopa Mulungu ochokera ku mayiko onse a dziko lapansi
ankakhala mu Yerusalemu nthawi imeneyi. [6] Utamveka mkokomo
uja, gulu la anthu linasonkhana. Anthuwo anadabwa chifukwa
aliyense anawamva atumwiwo akuyankhula ziyankhulo zosiyanasiyana.
[7] Mothedwa nzeru anafunsana kuti, "Kodi anthu onse amene akuyankhu-
lawa si Agalileya? [8] Nanga bwanji aliyense wa ife akuwamva iwo
mu chinenero cha kwawo? [9] Apanti, Amedi ndi Aelami; okhala ku
Mesopotamiya, ku Yudeya ndi ku Kapadokiya, ku Ponto ndi ku Asiya, [10] ku
Frugiya ndi Pamfiliya, ku Igupto ndi ku madera a ku Libiya kufupi ndi ku
Kurene; alendo ochokera ku Roma, [11] Ayuda ndi otsatira chipembedzo
cha Chiyuda onse pamodzi; Akrete ndi Aarabu, ife tonse tikuwamva
akuyankhula za ntchito zodabwitsa za Mulungu mu ziyankhulo zathu."
[12] Modabwa ndi mothedwa nzeru anafunsana wina ndi mnzake kuti,
"Zimenezi zikutanthauzanji?"
[13] Koma ena anawaseka nati, "Aledzera vinyo watsopano."

*Uthenga wa Petro*

[14] Koma Petro anayimirira pamodzi ndi atumwi khumi ndi mmodziwo
ndipo anakweza mawu ake nayankhula kwa gulu la anthu nati: "Ayuda
anzanga, ndi nonse amene muli mu Yerusalemu, mvetsetsani izi ndipo
tcherani khutu ku zimene ndikunena. [15] Kunena zoona, anthu awa

sanaledzere ayi, monga momwe mukuganizira, pakuti ino ndi 9 koloko
mmawa! 16 Koma izi ndi zimene ananena Mneneri Yoweli kuti:
17 " 'Mulungu akuti, m'masiku otsiriza
ndidzakhuthulira Mzimu wanga pa anthu onse.
Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera,
anyamata anu adzaona masomphenya,
nkhalamba zanu zidzalota maloto.
18 Ngakhalenso pa antchito anga aamuna ndi aakazi,
ndidzakhuthulira Mzimu wanga masiku amenewo,
ndipo iwo adzanenera.
19 Ndipo ndidzaonetsa zodabwitsa mlengalenga
ndi zizindikiro pa dziko lapansi pano,
ndizo magazi, moto ndi utsi watolotolo.
20 Dzuwa lidzadetsedwa
ndipo mwezi udzaoneka ngati magazi
lisanafike tsiku lalikulu ndi laulemerero la Ambuye.
21 Ndipo aliyense amene adzayitana
pa dzina la Ambuye adzapulumuka.'
22 "Inu Aisraeli mverani mawu awa; Yesu wa ku Nazareti anali
munthu amene anaperekedwa kwa inu ndi Mulungu. Ndipo Mulungu
anakutsimikizirani zimenezi ndi zamphamvu, zodabwitsa ndi zizindikiro
zimene anachita mwa Iye pakati panu, monga inu mukudziwa. 23 Yesu
ameneyu anaperekedwa kwa inu mwa kufuna ndi kudziwiratu kwa
Mulungu; ndipo inu mothandizidwa ndi anthu oyipa, munamupha Iye
pomupachika pa mtanda. 24 Koma Mulungu anamuukitsa kwa akufa,
kumumasula Iye ku zowawa za imfa, chifukwa kunali kosatheka kuti
agwiridwe ndi imfa. 25 Pakuti Davide ananena za Iye kuti,
" 'Ndinaona Ambuye pamaso panga nthawi zonse.
Chifukwa Iye ali kudzanja langa lamanja,
Ine sindidzagwedezeka.
26 Chifukwa chake mtima wanga ndi wokondwa ndipo lilime langa
likukondwera;
thupi langanso lidzakhala ndi chiyembekezo.
27 Chifukwa simudzasiya moyo wanga kumalo a anthu akufa, ku manda,
kapena kulekerera Woyerayo kuti awole.
28 Inu munandidziwitsa ine njira zamoyo;
Inu mudzandidzaza ndi chimwemwe pamaso panu.'
29 "Abale, ine ndikuwuzani motsimikiza kuti kholo lathu Davide
anamwalira ndipo anayikidwa m'manda, ndipo manda ake alipo lero lino.
30 Koma iye anali mneneri ndipo anadziwa kuti Mulungu analonjeza ndi
lumbiro kuti adzayika mmodzi wa zidzukulu zake pa mpando waufumu.
31 Davide ataoneratu zimene zinali m'tsogolo anayankhula za kuuka kwa
Khristu, kuti Iye sanasiyidwe m'manda, ndipo thupi lake silinawole.
32 Mulungu wamuukitsa Yesu ameneyu, ndipo ife ndife mboni za zimenezi.
33 Khristu anakwezedwa kukhala kudzanja lamanja la Mulungu, nalandira
Mzimu Woyera amene Atate anamulonjeza, ndipo watipatsa ife zimene
mukuona ndi kumvazi. 34 Pakuti si Davide anakwera kumwamba koma
iye akuti,
" 'Ambuye anawuza Ambuye anga kuti:
Khala kudzanja langa lamanja
35 mpaka nditasandutsa adani ako

kukhala chopondapo mapazi ako.'

36 "N'chifukwa chake, Aisraeli onse adziwe ndithu kuti, Yesu amene inu munamupachika, Mulungu wamuyika kukhala Ambuye ndiponso Mpulumutsi."

37 Anthu atamva zimenezi, anatsutsika kwambiri mu mtima ndipo anati kwa Petro ndi atumwi enawo, "Abale, kodi ife tichite chiyani?"

38 Petro anawayankha kuti, "Lapani ndipo mubatizidwe aliyense wa inu, m'dzina la Yesu Khristu kuti machimo anu akhululukidwe. Ndipo
mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera. 39 Pakuti lonjezoli ndi lanu ndi
ana anu ndiponso la onse amene ali kutali, ndi iwo onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitane."

40 Petro anawachenjeza ndi mawu ena ambiri, ndipo anawadandaulira
iwo kuti, "Mudzipulumutse ku m'bado owonongeka uno." 41 Iwo amene
anawulandira uthenga wake anabatizidwa ndipo tsiku lomwelo miyoyo pafupifupi 3,000 inawonjezedwa ku gulu lawo.

### *Kuyanjana kwa Okhulupirira*

42 Iwo ankasonkhana pamodzi kuphunzitsidwa ndi atumwi, pachiyan-
jano, pachakudya ndi popemphera. 43 Aliyense ankachita mantha chi-
fukwa cha zodabwitsa ndi zizindikiro zambiri zimene atumwi ankachita.
44 Okhulupirira onse anali pamodzi ndipo aliyense ankapereka zinthu zake
kuti zikhale za onse. 45 Ankagulitsa minda yawo ndi katundu wawo, ndi
kugawira kwa aliyense molingana ndi zosowa zake. 46 Tsiku ndi tsiku
ankasonkhana pamodzi pa bwalo la pa Nyumba ya Mulungu. Ankadya
pamodzi m'nyumba zawo mwasangala ndi mtima woona. 47 Ankayamika
Mulungu ndipo anthu onse ankawakomera mtima. Ndipo tsiku ndi tsiku Ambuye ankawonjezera ena pa chiwerengero cha olandira chipulumutso.

## 3

### *Petro Achiritsa Wolumala Miyendo*

1 Tsiku lina Petro ndi Yohane ankapita ku Nyumba ya Mulungu
kukapemphera nthawi ya 3 koloko masana. 2 Ndipo munthu wolumala
chibadwire ankanyamulidwa tsiku ndi tsiku kukayikidwa pa khomo la Nyumbayo lotchedwa Khomo Lokongola kuti azikapempha amene
amalowa ku bwalo la Nyumbayo. 3 Ataona Petro ndi Yohane ali
pafupi kulowa anawapempha ndalama. 4 Iwo anamuyang'anitsitsa iye.
Kenaka Petro anati, "Tiyang'ane!" 5 Munthuyo anawayang'anitsitsa
kuyembekezera kuti alandira kanthu kuchokera kwa iwo.

6 Petro anati kwa iye, "Ine ndilibe siliva kapena golide, koma chimene ndili nacho ndikupatsa. M'dzina la Yesu Khristu wa ku Nazareti, yenda."
7 Ndipo anamugwira dzanja lamanja, namuthandiza kuti ayimirire ndipo
nthawi yomweyo mapazi ake ndi akakolo ake analimba. 8 Iye analumpha
ndi kuyamba kuyenda. Kenaka analowa nawo pamodzi m'bwalo la Nyumba ya Mulungu, akuyenda ndi kulumpha ndiponso kuyamika
Mulungu. 9 Anthu onse atamuona akuyenda ndiponso kuyamika Mulungu,
10 anamuzindikira kuti ndi yemwe uja ankakhala pa khomo la Nyumbayo lotchedwa Khomo Lokongola, ndipo anazizwa ndi kudabwa ndi zimene zinamuchitikira.

### *Petro Ayankhula kwa Anthu*

11 Wopempha uja akuyenda pamodzi ndi Petro ndi Yohane, anthu
onse anadabwa ndipo anawathamangira iwo kumalo wotchedwa Khonde
la Solomoni. 12 Petro ataona zimenezi anawawuza kuti, “Inu Ais-
raeli, chifukwa chiyani mukudabwa ndi zimene zachitikazi? Bwanji
mukuyang’ana ife ngati kuti tamuyendetsa munthuyu ndi mphamvu
yathu kapena chifukwa cha kupembedza kwathu? 13 Mulungu wa
Abrahamu, Isake ndi Yakobo, Mulungu wa makolo athu, wamulemekeza
mtumiki wake Yesu. Amene inu munamukana pamaso pa Pilato ndi kumu-
pereka Iye kuti aphedwe, ngakhale kuti Pilato anafuna kuti amumasule.
14 Koma inu munamukana Woyera ndi Wolungamayo ndipo munapempha
kuti akumasulireni munthu wakupha anthu. 15 Inu munapha mwini
moyo, koma Mulungu anamuukitsa kwa akufa. Ife ndife mboni za
zimenezi. 16 Mwachikhulupiriro m’dzina la Yesu, munthu uyu amene
mukumuona ndi kumudziwa analimbikitsidwa. M’dzina la Yesu ndi
chikhulupiriro chimene chili mwa iye chamuchiritsa kwathunthu, monga
nonse mukuona.
17 “Tsopano abale ine ndikudziwa kuti inu munachita zimenezi
mosadziwa, monga momwenso anachitira atsogoleri anu. 18 Koma
umu ndi mmene Mulungu anakwaniritsira zimene zinanenedwa kale
ndi aneneri onse, kuti Khristu adzamva zowawa. 19 Chifukwa chake,
lapani, bwererani kwa Mulungu, kuti machimo anu afafanizidwe, kuti
nthawi ya kutsitsimuka ibwere kuchokera kwa Ambuye, 20 ndi kuti Iye
atumize Yesu Khristu amene anasankhidwa chifukwa cha inu. 21 Iye
ayenera kukhalabe kumwamba mpaka nthawi ya kukonzanso zinthu
zonse monga Mulungu analonjeza kale kudzera mwa aneneri ake oyera
mtima. 22 Pakuti Mose anati, ‘Ambuye Mulungu wanu adzakuukitsirani
mneneri monga ine kuchokera pakati pa anthu anu; mumvere zonse
zimene iye akuwuzeni. 23 Aliyense amene sadzamvera mawu a mnener-
iyo, adzayenera kuchotsedwa pakati pa abale ake.’
24 “Ndipo aneneri onse ambiri amene anayankhula kuyambira Samueli,
ananeneratu za masiku ano. 25 Inu ndinu ana a aneneri ndiponso
ana apangano limene Mulungu anachita ndi makolo anu. Iye anati
kwa Abrahamu, ‘Anthu onse a pa dziko lapansi adzadalitsika kudzera
mwa zidzukulu zako.’ 26 Pamene Mulungu anaukitsa mtumiki wake,
anamutuma Iye poyamba kwa inu kuti akudalitseni pobweza aliyense wa
inu ku zoyipa zake.”

# 4

*Petro ndi Yohane ku Bwalo la Akulu*

1 Pamene Petro ndi Yohane amayankhula ndi anthu, kunabwera
ansembe, mkulu woyang’anira Nyumba ya Mulungu ndiponso Asaduki.
2 Iwo anakhumudwa kwambiri chifukwa atumwiwo amaphunzitsa anthu
ndi kumalalikira za kuuka kwa akufa mwa Yesu. 3 Iwo anagwira Petro
ndi Yohane, popeza kunali kutada, anawayika m’ndende mpaka mmawa
mwake. 4 Koma anthu ambiri amene anamva uthenga anakhulupirira,
ndipo chiwerengero cha anthu chinakwana 5,000.
5 Mmawa mwake olamulira, akulu ndi aphunzitsi a malamulo ana-
sonkhana mu Yerusalemu. 6 Panali Anasi, Mkulu wa ansembe, Kayafa,
Yohane ndi Alekisandro ndi ana a banja la mkulu wa ansembe. 7 Iwo
anayimiritsa Petro ndi Yohane patsogolo pawo nayamba kuwafunsa kuti,
“Kodi munachita zimenezi ndi mphamvu yanji kapena m’dzina la yani?”

8 Petro wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, anawawuza kuti, "Inu ola-
mulira ndi akulu! 9 Ngati ife tikufunsidwa lero chifukwa cha ntchito
yabwino imene yachitika pa munthu wolumala miyendo ndi mmene
iye anachiritsidwira, 10 tsono dziwani izi inu ndi aliyense mu Israeli:
munthuyu akuyima pamaso panu, wochiritsidwa kwathunthu, ndi chi-
fukwa cha dzina la Yesu Khristu wa ku Nazareti amene munamupachika
koma Mulungu anamuukitsa kwa akufa. 11 Iye ndi

" 'Mwala umene amisiri omanga nyumba anawukana,
umenewo wasanduka mwala wa pa ngodya!'

12 Chipulumutso sichipezeka mwa wina aliyense; pakuti palibe dzina
lina pansi pa thambo limene lapatsidwa kwa anthu limene tiyenera
kupulumutsidwa nalo."

13 Ataona kulimba mtima kwa Petro ndi Yohane ndi kuzindikira kuti
anali osaphunzira, anthu wamba, anadabwa kwambiri ndipo anazindikira
kuti anthuwa anakhala pamodzi ndi Yesu. 14 Koma popeza iwo amamuona
munthu amene anachiritsidwa atayima pamodzi ndi iwo, palibe chimene
akananena. 15 Chifukwa chake anawalamula kuti atuluke m'bwalo
la milandu ndipo akulu abwalowo anayamba kukambirana. 16 Iwo
anafunsana kuti, "Kodi anthuwa tichite nawo chiyani? Pakuti aliyense
okhala mu Yerusalemu akudziwa kuti achita chodabwitsachi, ndipo ife
sitingathe kukana. 17 Koma kuti mbiriyi isapitirire kuwanda pakati pa
anthu, ife tiwachenjeze anthu amenewa kuti asayankhulenso kwa wina
aliyense m'dzina la Yesu."

18 Pamenepo anawayitananso ndipo anawalamula kuti asayankhule
kapena kuphunzitsa konse m'dzina la Yesu. 19 Koma Petro ndi Yohane
anayankha kuti, "Weruzani nokha ngati n'kwabwino pamaso pa Mulungu
kumvera inu koposa Mulungu. 20 Ife sitingaleke kuyankhula za zimene
tinaziona ndi kuzimva."

21 Atawonjeza kuwaopseza anawamasula. Sanathe kugwirizana njira
yowalangira, chifukwa anthu onse amayamika Mulungu chifukwa cha
zimene zinachitika. 22 Ndipo munthu amene anachiritsidwayo anali ndi
zaka makumi anayi.

### *Okhulupirira Apemphera*

23 Atamasulidwa Petro ndi Yohane anapita kwa anzawo ndipo anawafo-
tokozera zonse zimene akulu a ansembe ndi akulu anawawuza. 24 Anthu
atamva zimenezi anafuwula ndi mtima umodzi napemphera kwa Mu-
lungu. Iwo anati, "Ambuye wolamulira zonse, Inu munalenga kumwamba
ndi dziko lapansi ndi nyanja ndiponso zonse zili m'menemo. 25 Inu
munayankhula mwa Mzimu Woyera kudzera pakamwa pa Davide kholo
lathu, mtumiki wanu kuti,

" 'N'chifukwa chiyani anthu a mitundu ina akufuna kuchita chiwembu,
ndipo akonzekera kuchita zopandapake?

26 Mafumu a dziko lapansi akugwirizana nazo;
ndipo olamulira asonkhana pamodzi
kulimbana ndi Ambuye
ndi wodzozedwa wakeyo.'

27 Zoonadi, Herode ndi Pontiyo Pilato anasonkhana pamodzi ndi amitundu
ndiponso Aisraeli, mu mzinda muno, kupanga zolimbana ndi mtumiki
wanu woyera Yesu, amene Inu munamudzoza. 28 Iwo anachita zimene
munakonzeratu mwachifuniro chanu ndi mphamvu yanu kuti zichitike.
29 Tsopano, Ambuye taonani kuti atiopseza, tithandizeni ife atumiki anu,

kuti tiyankhule mawu anu molimba mtima. 30 Tambasulani dzanja lanu
kuchiritsa anthu ndipo kuti, zizindikiro zodabwitsa zichitike m'dzina la
mtumiki wanu woyera Yesu."
31 Iwo atatha kupemphera, malo amene anasonkhanapo anagwedezeka.
Ndipo iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo anayankhula
Mawu a Mulungu molimba mtima.

### *Okhulupirira Agawana Zinthu Zawo*

32 Okhulupirira onse anali a mtima umodzi, ndi maganizo amodzi.
Palibe munthu amene amati zomwe anali nazo zinali zake zokha, koma
amagawana chilichonse chimene anali nacho. 33 Atumwi anapitirira
kuchitira umboni mwa mphamvu zakuuka kwa Ambuye Yesu, ndipo pa
iwo panali chisomo chochuluka. 34 Panalibe anthu osowa kanthu pakati
pawo. Pakuti amene anali ndi malo, kapena nyumba amagulitsa ndi kub-
weretsa ndalamazo 35 ndi kuzipereka kwa atumwi, ndipo zimagawidwa
kwa aliyense amene anali ndi chosowa.
36 Yosefe, wa fuko la Levi, wochokera ku Kupro amene atumwi ana-
mutcha Barnaba, kutanthauza kuti mwana wachilimbikitso, 37 anagulitsa
munda wake ndipo anadzapereka ndalamazo kwa atumwi.

## 5

### *Hananiya ndi Safira*

1 Koma munthu wina dzina lake Hananiya, pamodzi ndi mkazi wake
Safira, anagulitsanso munda wawo. 2 Mogwirizana ndi mkazi wakeyo
anapatulapo pa ndalamazo nazisunga, ndipo anatenga zotsalazo ndi
kukapereka kwa atumwi.
3 Koma Petro anamufunsa kuti, "Hananiya, chifukwa chiyani Satana
anadzaza chotere mu mtima wako kuti unamize Mzimu Woyera ndipo
wapatula ndi kusunga ndalama? 4 Kodi sunali wako usanagulitse?
Ndipo utagulitsa ndalamazo sizinali m'manja mwako kodi? N'chiyani
chinakuchititsa zimenezi? Iwe sunanamize anthu koma Mulungu."
5 Hananiya atamva mawu amenewa anagwa pansi namwalira. Onse
amene anamva zimene zinachitikazi anachita mantha kwambiri. 6 Kenaka
anyamata anafika, nakulunga thupi lake, ndipo anamunyamula ndi
kukamuyika m'manda.
7 Patapita maora atatu mkazi wake analowa, wosadziwa zimene zina-
chitika. 8 Petro anamufunsa iye kuti, "Tandiwuza, kodi izi ndi ndalama
zonse zimene iwe ndi Hananiya munalandira mutagulitsa munda?"
Mkaziyo anati, "Inde ndi zimenezo."
9 Petro anati kwa iye, "Bwanji inu munapangana kuyesa Mzimu wa
Ambuye? Taona! Anthu amene anakayika mwamuna wako m'manda ali
pa khomo, ndipo adzakunyamula iwenso."
10 Nthawi yomweyo anagwa pansi pa mapazi a Petro ndipo anamwalira.
Ndipo anyamata aja analowa, napeza kuti wafa kale, anamunyamula ndi
kukamuyika pafupi ndi mwamuna wake. 11 Mpingo wonse ndi anthu onse
amene anamva zimenezi anachita mantha kwambiri.

### *Atumwi Achiritsa Anthu Ambiri*

12 Atumwi anachita zizindikiro zodabwitsa ndi zozizwitsa zambiri
pakati pa anthu. Ndipo onse okhulupirira ankasonkhana pamodzi mu
Khonde la Solomoni. 13 Palibe ndi mmodzi yemwe analimba mtima
kuphatikana nawo, ngakhale kuti anthu onse amawalemekeza kwambiri.

14 Ngakhale zinali chotere, anthu ambiri anakhulupirira Ambuye ndipo
amawonjezeredwa ku chiwerengero chawo. 15 Chifukwa cha zimenezi,
anthu anabweretsa odwala m'misewu ya mu mzinda nawagoneka pa
mabedi ndi pa mphasa kuti chithunzi chokha cha Petro chikhudze ena
mwa iwo iye akamadutsa. 16 Anthu ochuluka ochokera ku mizinda
yaying'ono ozungulira Yerusalemu amasonkhananso atatenga odwala
awo ndi iwo amene amasautsidwa ndi mizimu yoyipa ndipo onsewo
amachiritsidwa.

### *Atumwi Azunzidwa*

17 Koma mkulu wa ansembe pamodzi ndi onse omuthandiza, amene
anali a gulu la Asaduki, anachita nsanje. 18 Iwo anagwira atumwi ndi
kuwatsekera m'ndende ya anthu wamba. 19 Koma usiku mngelo wa
Ambuye anatsekula zitseko za ndende ndi kuwatulutsa 20 Mngeloyo anati,
"Pitani, ku mabwalo a Nyumba ya Mulungu ndipo mukawuze anthu
uthenga onse wamoyo watsopanowu."

21 Kutacha mmawa, atumwi analowa m'bwalo la m'Nyumba ya Mu-
lungu, monga anawuzidwa ndipo anayamba kuphunzitsa anthu.

Mkulu wa ansembe pamodzi ndi omuthandiza ake amene anali naye
anafika, anayitanitsa msonkhano wa Bwalo Lalikulu, ndilo bwalo la akulu
onse a Israeli. Anatuma alonda kuti akatenge atumwi aja kundende.
22 Koma alonda aja atafika kundende, sanawapezemo. Iwo anabwerera
nakawafotokozera 23 kuti, "Tinakapeza ndende ili chitsekere ndithu,
ndi alonda atayimirira pa khomo, koma pamene tinatsekula zitseko,
sitinapezemo munthu aliyense m'katimo." 24 Mkulu wa alonda a Nyumba
ya Mulungu ndi akulu a ansembe atamva zimenezi anathedwa nzeru,
osadziwa kuti zimenezi zidzatha bwanji.

25 Ndipo wina anabwera ndi kuti, "Taonani! Anthu aja amene mu-
nawatsekera m'ndende ali ku Nyumba ya Mulungu ndipo akuphunzitsa
anthu." 26 Pamenepo mkulu wa alonda pamodzi ndi alonda anakawa-
tenga atumwi. Sanakawatenge mwaukali, chifukwa amaopa kuti anthu
angawaponye miyala.

27 Atafika nawo atumwi aja, anawayimika pamaso pa Bwalo Lalikulu
kuti afunsidwe mafunso ndi mkulu wa ansembe. 28 Iye anati, "Ife
tinakuletsani kuti musaphunzitsenso m'dzina ili, koma inu mwadzaza
Yerusalemu ndi chiphunzitso chanu, ndipo mukufuna kutisenzetsa imfa
ya munthu ameneyu."

29 Petro ndi atumwi enawo anayankha kuti, "Ife tiyenera kumvera Mu-
lungu osati anthu! 30 Mulungu wa makolo athu anamuukitsa Yesu, amene
inu munamupha pomupachika pa mtengo. 31 Mulungu anamukweza Iye
ku dzanja lake lamanja kukhala Mfumu ndi Mpulumutsi kuti Iye apatse
Aisraeli mtima wolapa ndi chikhululukiro cha machimo. 32 Ife ndife mboni
za zimenezi, ndiponso Mzimu Woyera amene Mulungu anapereka kwa
iwo akumvera Iye."

33 Akuluakuluwo atamva zimenezi anakwiya kwambiri nafuna
kuwapha. 34 Koma Mfarisi wina dzina lake Gamalieli, mphunzitsi wa
malamulo, amene anthu onse amamulemekeza, anayimirira ndi kulamula
kuti atumwiwo ayambe apita panja. 35 Ndipo iye anawuza bwalolo kuti,
"Aisraeli, taganizani bwino, zimene mukufuna kuchita kwa anthu awa.
36 Pakuti masiku a m'mbuyomu kunali Teuda amene anadzitchukitsa,
ndipo anthu pafupifupi 400 anamutsatira. Iye anaphedwa ndipo

omutsatira akewo anabalalitsidwa, zonse zinatheratu. 37 Pambuyo pake,
nthawi ya kalembera kunalinso Yudasi wa ku Galileya, ndipo anatsogolera
gulu la anthu amene anawukira, iyenso anaphedwa ndipo anthu ake onse
anabalalitsidwa. 38 Chifukwa chake pa nkhani iyi ndikuwuzani kuti,
alekeni anthuwa ndipo aloleni apite! Pakuti ngati zimene akuganiza
kapena kuchita ndi zochokera kwa munthu zidzalephera. 39 Koma ngati
ndi zochokera kwa Mulungu inu simudzatha kuwaletsa anthu awa: inu
mwina muzapezeka kuti mukulimbana ndi Mulungu."

40 Akuluakulu enawo anavomerezana naye. Iwo anayitana atumwi aja
ndipo anawakwapula kwambiri. Ndipo anawalamula kuti asayankhu-
lenso m'dzina la Yesu ndipo anawamasula.

41 Iwo anachoka ku Bwalo Lalikulu akukondwa chifukwa anayesedwa
oyenera kunyozedwa chifukwa cha dzina la Yesu. 42 Ndipo tsiku ndi tsiku,
sanaleke kuphunzitsa ndi kulalikira m'Nyumba ya Mulungu komanso
nyumba ndi nyumba, Uthenga Wabwino wa kuti Yesu ndi Khristu.

# 6

### *Asankha Atumiki Asanu ndi Awiri*

1 M'masiku amenewo pamene chiwerengero cha ophunzira chinkachu-
luka, Ayuda a Chihelene pakati pawo anadandaula chifukwa cha Ayuda a
Chihebri chifukwa amasiye awo samawagawira chakudya cha tsiku ndi
tsiku. 2 Tsono Atumwi khumi ndi awiriwo anasonkhanitsa ophunzira
onse pamodzi ndipo anati, "N'kosayenera kuti ife tisiye kulalikira Mawu
a Mulungu ndi kuyang'anira za chakudya. 3 Choncho abale, sankhani
pakati panu anthu asanu ndi awiri a mbiri yabwino, odzazidwa ndi Mzimu
Woyera ndi anzeru. Ife tidzawapatsa udindo oyang'anira. 4 Koma ife
tidzadzipereka kuti tizipemphera ndi kulalikira mawu."

5 Mawu amenewa anakondweretsa gulu lonse la anthu. Iwo anasankha,
Stefano, munthu wodzazidwa ndi chikhulupiriro ndiponso Mzimu Woy-
era; anasankhanso Filipo, Prokoro, Nikanora, Timo, Parmena ndi Nikolao
amene anatembenuka mtima ndi kulowa Chiyuda kuchokera kwa An-
tiokeya. 6 Iwo anapereka anthuwa kwa atumwi amene anawapempherera
ndi kuwasanjika manja.

7 Ndipo Mawu a Mulungu anapitirira kufalikira. Chiwerengero cha
ophunzira mu Yerusalemu chinakula mofulumira ndipo ansembe ochu-
luka anakhulupirira.

### *Ayuda Agwira Stefano*

8 Stefano, munthu wodzazidwa ndi chisomo cha Mulungu ndi mphamvu
anachita zodabwitsa ndiponso zizindikiro zazikulu pakati pa anthu.
9 Panauka mtsutso kuchokera kwa anthu a ku Kurene ndi a ku Alek-
isandriya komanso a ku dera la Silisiya ndi Asiya, otchedwa a Sunagoge
ya Mfulu. Anthu amenewa anayamba kutsutsana ndi Stefano. 10 Koma
iwo sanathe kumugonjetsa chifukwa iye ankayankhula ndi nzeru zimene
Mzimu Woyera anamupatsa.

11 Iwo ananyengerera anthu ena mwamseri kuti anene kuti, "Ife tinamva
Stefano akuchitira chipongwe Mose ndiponso Mulungu."

12 Motero anawutsa mitima ya anthu, akulu ndi aphunzitsi amalamulo.
Anamugwira Stefano ndi kumubweretsa ku Bwalo Lalikulu. 13 Iwo
anabweretsa mboni zonama zimene zinati, "Munthu uyu akupitirirabe
kuyankhula mawu onyoza malo oyera ndi malamulo. 14 Pakuti tinamumva

akunena kuti Yesu uja wa ku Nazareti adzawononga malo ano ndiponso
kusintha miyambo imene Mose anatipatsa.”
15 Onse amene anakhala pansi M’bwalo Lalikulu anamuyang’anitsitsa
Stefano, ndipo anaona kuti nkhope yake ikuwala ngati ya mngelo.

# 7

*Mawu a Stefano*

1 Kenaka mkulu wa ansembe anafunsa Stefano kuti, “Kodi zimene
akukunenerazi ndi zoona?”
2 Stefano anayankha kuti, “Abale ndi makolo, tamverani! Mulungu
waulemerero anaoneka kwa kholo lathu Abrahamu pamene ankakhala
ku Mesopotamiya, asanakakhale ku Harani. 3 Mulungu anati, ‘Tuluka
m’dziko lako, siya abale ako, ndipo pita ku dziko limene ndidzakusonyeza.’
4 “Ndipo iye anatulukadi m’dziko la Akaldeya ndi kukakhala ku
Harani. Atamwalira abambo ake, Mulungu anamuchotsa kumeneko
ndi kumubweretsa m’dziko lino limene inu mukukhalamo tsopano.
5 Mulungu sanamupatse cholowa kuno, ngakhale kadera kakang’ono
kadziko. Koma Mulungu anamulonjeza kuti adzapereka dziko lino kwa iye
ndi kwa zidzukulu zake, ngakhale kuti pa nthawi imeneyi analibe mwana.
6 Mulungu anayankhula motere kwa iye: ‘Zidzukulu zako zidzakhala
alendo m’dziko lachilendo, ndipo zidzakhala akapolo ndi kuzunzidwa
zaka 400.’ 7 Mulungu anati, ‘Ine ndidzalanga dziko limene zidzukulu
zako zidzagwireko ukapolo, ndipo pambuyo pake akadzatuluka m’dzikolo
adzandipembedza Ine pamalo pano.’ 8 Kenaka Mulungu anachita pangano
la mdulidwe ndi Abrahamu. Ndipo Abrahamu, anabereka Isake, na-
mudula ali ndi masiku asanu ndi atatu. Ndipo Isake anabereka Yakobo,
Yakobo anabereka makolo khumi ndi awiri aja.
9 “Makolo athu anachita nsanje ndi Yosefe ndipo anamugulitsa kuti
akakhale kapolo ku Igupto. Koma Mulungu anali naye 10 ndipo anamupu-
lumutsa iye kumasautso ake onse. Mulungu anamupatsa Yosefe nzeru
ndi chisomo pamaso pa Farao mfumu ya ku Igupto, kotero mfumuyo
inamuyika iye kukhala nduna yayikulu ya dziko la Igupto ndiponso
nyumba yake yonse yaufumu.
11 “Kenaka munalowa njala m’dziko la Kanaani, kotero kuti anthu
anavutika kwambiri, ndipo makolo athu sanathe kupeza chakudya.
12 Pamene Yakobo anamva kuti ku Igupto kunali tirigu, iye anatuma
makolo athu ulendo woyamba. 13 Pa ulendo wawo wachiwiri, Yosefe
anadziwulula kwa abale akewo ndipo Farao anadziwa za banja la Yosefe.
14 Izi zinachitika, Yosefe anayitanitsa abambo ake Yakobo ndi banja lonse,
onse pamodzi analipo 75. 15 Motero Yakobo anapita ku Igupto, kumene iye
ndiponso makolo athu anamwalira. 16 Mitembo yawo anayinyamula ndi
kupita nayo ku Sekemu kumene inayikidwa m’manda amene Abrahamu
anagula kochokera kwa ana a Hamori ku Sekemuko.
17 “Nthawi itayandikira yakuti Mulungu achite zimene analonjeza
kwa Abrahamu, mtundu wathu unakula ndi kuchuluka kwambiri mu
Igupto. 18 Pambuyo pake mfumu yatsopano imene sinkamudziwa Yosefe,
inayamba kulamulira dziko la Igupto. 19 Mfumuyo inachita mwachinyengo
ndi mtundu wathu ndi kuwazunza kuti ataye ana awo akhanda kuti afe.
20 “Pa nthawi imeneyo Mose anabadwa, ndipo anali wokongola
kwambiri. Iye analeredwa m’nyumba ya abambo ake kwa miyezi itatu.

21 Atakamutaya, mwana wamkazi wa Farao anamutola nakamulera ngati
mwana wake. 22 Mose anaphunzira nzeru zonse za Aigupto, ndipo anali
wamphamvu m'mawu ndi ntchito zake.
23 "Mose ali ndi zaka makumi anayi, anaganizira zokayendera abale
ake Aisraeli. 24 Iye ataona mmodzi wa iwo akuzunzidwa ndi Mwigupto,
anatchinjiriza Mwisraeliyo, namupha Mwiguptoyo. 25 Mose anaganiza
kuti abale ake adzazindikira kuti Mulungu anamuyika kuti awapulumutse
koma iwo sanazindikire. 26 Mmawa mwake Mose anaona Aisraeli awiri
akukangana. Iye anayesa kuwayanjanitsa ponena kuti, 'Amuna inu, ndinu
abale; chifukwa chiyani mukufuna kupwetekana?'
27 "Koma munthu amene amavutitsa mnzakeyo anakankha Mose ndipo
anati, 'Ndani anakuyika kuti ukhale wotilamulira ndi wotiweruza. 28 Kodi
ukufuna kundipha monga momwe unaphera Mwigupto uja dzulo?'
29 Mose atamva mawu awa anathawira ku Midiyani, kumene anakhala
mlendo ndipo anabereka ana amuna awiri.
30 "Ndipo patapita zaka makumi anayi mngelo anaonekera kwa Mose
m'malawi amoto pa chitsamba m'chipululu pafupi ndi Phiri la Sinai.
31 Iye ataona zimenezi, anadabwa. Akupita kuti akaonetsetse pafupi, Mose
anamva mawu a Ambuye: 32 'Ine ndine Mulungu wa makolo ako, Mulungu
wa Abrahamu, Isake ndi Yakobo.' Mose ananjenjemera chifukwa cha
mantha ndipo sanalimbe mtima kuyang'ananso.
33 "Ndipo Ambuye anati kwa Mose, 'Vula nsapato zako, pakuti malo
amene wayimapo ndi opatulika. 34 Ine ndaona ndithu mazunzo a anthu
anga amene ali ku Igupto. Ndamva kulira kwawo choncho ndabwera kuti
ndiwapulumutse. Tsopano tiye ndikutume ku Igupto.'
35 "Uyu ndi Mose yemwe uja amene Aisraeli anamukana ndi kunena
kuti, 'Ndani anakuyika kuti ukhale wotilamulira ndi wotiweruza?' Iyeyo
anatumidwa ndi Mulungu mwini kuti akakhale wowalamulira ndiponso
mpulumutsi, mothandizidwa ndi mngelo amene anamuonekera pa chit-
samba. 36 Iye anawatulutsa mu Igupto ndipo anachita zodabwitsa ndi
zizindikiro zozizwitsa mu Igupto, pa Nyanja Yofiira, ndiponso m'chipululu
kwa zaka makumi anayi.
37 "Uyu ndi Mose uja amene anati kwa Aisraeli, 'Mulungu adzawutsa
pakati pa abale anu mneneri ngati ine.' 38 Iyeyu anali m'gulu la Aisraeli
m'chipululu pamodzi ndi mngelo amene anamuyankhula pa phiri la Sinai
ndiponso makolo athu; ndipo Mose analandira mawu amoyo kuti atipatse
ife.
39 "Koma makolo athu anakana kumumvera iye. Iwo anamukana
iye ndipo m'mitima mwawo anatembenukira ku Igupto. 40 Iwo anati
kwa Aaroni, 'Bwera utipangire milungu imene idzititsogolera. Kunena
za Mose amene anatitsogolera kutuluka m'dziko la Igupto, sitikudziwa
chimene chamuchitikira. 41 Iyi ndi nthawi imene anapanga fano la mwana
wang'ombe. Anapereka nsembe kwa fanoli nachita chikondwerero
kulemekeza ntchito ya manja awo. 42 Koma Mulungu anawafulatira,
nawapereka kuti apembedze zolengedwa zakumwamba. Zimenezi zikug-
wirizana ndi zimene zinalembedwa m'buku la aneneri kuti,
" 'Kodi pa zaka makumi anayi zimene munakhala m'chipululu muja
munkandibweretsera nsembe ndi zopereka, inu nyumba ya Israeli?'
43 Ayi, inu mwanyamula tenti ya Moloki
ndi nyenyezi ya mulungu wanu Refani,
mafano amene munapanga kuti muziwapembedza.

Chifukwa chake, Ine ndidzakutumizani kutali, kupitirira dziko la Babuloni.
44 “Makolo athu anali ndi tenti ya msonkhano pakati pawo m’chipululu.
Anayipanga monga momwe Mulungu anawuzira Mose, molingana ndi
chithunzi chimene Mose anachiona. 45 Makolo athu, atayilandira Tentiyo,
anabwera nayo motsogozedwa ndi Yoswa pamene analanda dziko la
mitundu imene Mulungu anayipirikitsa pamaso pawo. Tentiyo inakhala
m’dzikomo mpaka nthawi ya Davide, 46 amene anapeza chisomo pamaso
pa Mulungu ndipo anapempha kuti am’mangire nyumba Mulungu wa
Yakobo. 47 Koma anali Solomoni amene anamanga nyumbayo.
48 “Komatu, Wammwambamwambayo sakhala m’nyumba zomangidwa
ndi anthu. Monga mneneri akunena kuti,

49 “ ‘Kumwamba ndi mpando wanga waufumu,
ndipo dziko lapansi ndi chopondapo mapazi anga.
Kodi mudzandimangira nyumba yotani?
Akutero Ambuye.
Kapena malo opumuliramo Ine ali kuti?
50 Kodi si dzanja langa linapanga zonsezi?’

51 “Anthu wokanika inu, osachita mdulidwe wa mu mtima ndi a makutu
ogontha! Inu ofanana ndi makolo anu. Nthawi zonse mumakana
kumvera Mzimu Woyera: 52 Kodi analipo mneneri amene makolo anu
sanamuzunze? Iwo anapha ngakhale amene ananeneratu za kubwera
kwa Wolungamayo. Ndipo tsopano inu munamupereka ndi kumupha Iye.
53 Inu amene munalandira Malamulo amene anaperekedwa ndi angelo
ndipo simunawamvere.”

### *Kuphedwa kwa Stefano*

54 Atamva zimenezi, iwo anakwiya kwambiri ndipo anamukukutira
mano. 55 Koma Stefano, wodzaza ndi Mzimu Woyera, anayang’ana
kumwamba ndipo anaona ulemerero wa Mulungu ndiponso Yesu atay-
imirira ku dzanja lamanja la Mulungu. 56 Stefano anati, “Taonani,
ndikuona kumwamba kotsekuka ndiponso Mwana wa Munthu atayimirira
ku dzanja la manja la Mulungu.”
57 Koma iwo anatseka m’makutu mwawo, ndipo anafuwula kolimba,
onse anathamangira kwa iye, 58 anamukokera kunja kwa mzinda ndipo
anayamba kumugenda miyala. Mboni zinasungitsa zovala zawo kwa
mnyamata otchedwa Saulo.
59 Akumugenda miyala, Stefano anapemphera kuti, “Ambuye Yesu,
landirani mzimu wanga.” 60 Ndipo anagwada pansi nafuwula
mwamphamvu kuti, “Ambuye musawawerengere tchimoli.” Atanena
mawu amenewa anamwalira.

## 8

1 Ndipo Saulo anavomerezana nawo pa imfa ya Stefano.

### *Kuzunzika kwa Mpingo*

Tsiku lomwelo, mpingo wa mu Yerusalemu unayamba kuzunzidwa,
ndipo onse, kupatulapo atumwi, anabalalikira ku madera onse a Yudeya
ndi Samariya. 2 Anthu okonda Mulungu anayika maliro a Stefano ndipo
anamulira kwambiri. 3 Koma Saulo anayamba kuwononga mpingo.
Amapita nyumba ndi nyumba, ndipo amagwira amuna ndi amayi ndi
kukawatsekera ku ndende.

### *Filipo ku Samariya*

4 Okhulupirira amene anabalalika amalalikira konse kumene amapita.
5 Filipo anapita ku mzinda wa ku Samariya ndipo analalikira za Khristu
kumeneko. 6 Gulu la anthu litamva Filipo akulalikira komanso kuona
zizindikiro zozizwitsa zimene ankazichita, onse anamvetsetsa zimene
iye amanena. 7 Mizimu yoyipa inatuluka mwa anthu ambiri ikufuwula
kwambiri ndipo ambiri amene anali akufa ziwalo ndi olumala anachirit-
sidwa. 8 Kotero munali chimwemwe chachikulu mu mzindawo.

### *Simoni Wamatsenga*

9 Koma mu mzindawo munali munthu dzina lake Simoni, amene
amachita za matsenga ndi kudabwitsa anthu a mu Samariya. Iye
amadzitamandira kuti ndi wopambana, 10 ndipo anthu onse, aakulu ndi
aang'ono anamumvera ndi kunena kuti, "Munthu uyu ndi mphamvu
ya Mulungu yotchedwa Mphamvu yayikulu." 11 Anthu amamutsata
chifukwa kwa nthawi yayitali amawadabwitsa ndi matsenga akewo.
12 Koma atakhulupirira Filipo akulalikira Uthenga Wabwino wa ufumu
wa Mulungu ndiponso dzina la Yesu Khristu, anthuwo anabatizidwa
amuna ndi amayi. 13 Nayenso Simoni anakhulupirira ndipo anabatizidwa,
natsatira Filipo kulikonse, ndipo anadabwa kwambiri pamene anaona
zizindikiro zazikulu ndi zozizwitsa.
14 Atumwi a ku Yerusalemu atamva kuti anthu a ku Samariya analandira
Mawu a Mulungu, anatumiza Petro ndi Yohane. 15 Atafika anawapem-
pherera kuti alandire Mzimu Woyera, 16 chifukwa Mzimu Woyera anali
asanafike pa wina aliyense wa iwo; anali atangobatizidwa m'dzina la
Ambuye Yesu. 17 Ndipo Petro ndi Yohane anasanjika manja awo pa iwo,
ndipo analandira Mzimu Woyera.
18 Simoni ataona kuti Mzimu anaperekedwa kwa iwo atumwi atawasan-
jika manja, iye anafuna kuwapatsa ndalama ndipo anati, 19 "Inenso
ndipatseni mphamvu imeneyi kuti aliyense amene ndimusanjika manja
anga azilandira Mzimu Woyera."
20 Petro anayankha kuti, "Ndalama zako utayike nazo pamodzi, chi-
fukwa unaganiza kuti ungathe kugula mphatso ya Mulungu ndi ndalama!
21 Ulibe gawo kapena mbali pa utumikiwu, chifukwa mtima wako suli
wolungama pamaso pa Mulungu. 22 Lapa zoyipa zakozi ndipo upemphere
kwa Ambuye. Mwina adzakukhululukira maganizo a mu mtima mwako.
23 Pakuti ine ndikuona kuti ndiwe wowawidwa mtima ndiponso kapolo
wa tchimo."
24 Ndipo Simoni anayankha, "Mundipempherere kwa Ambuye kuti
zisandigwere izi mwanenazi."
25 Atatha kuchitira umboni ndi kulalikira mawu a Ambuye, Petro ndi
Yohane anabwerera ku Yerusalemu, atalalikira Uthenga Wabwino m'midzi
yambiri ya Asamariya.

### *Filipo ndi Nduna ya Zachuma ya ku Etiopia*

26 Mngelo wa Ambuye anati kwa Filipo, "Nyamuka pita chakummwera,
ku msewu wa ku chipululu wopita ku Gaza kuchokera ku Yerusalemu."
27 Ndipo ananyamuka napita, ndipo akuyenda anakumana ndi munthu
wa ku Etiopia wa udindo waukulu woyang'anira chuma cha Kandake,
mfumu yayikazi ya ku Etiopia. Munthu ameneyu anapita ku Yerusalemu
kukapembedza Mulungu, 28 ndipo akubwerera kwawo atakwera pa galeta
lake amawerenga buku la mneneri Yesaya. 29 Mzimu anamuwuza Filipo
kuti, "Pita pa galeta ilo ndipo ukakhale pafupi nalo."

30 Pamenepo Filipo anathamangira ku galeta ndipo anamva munthuyo
akuwerenga buku la mneneri Yesaya. Filipo anamufunsa kuti, "Kodi
mukumvetsa zimene mukuwerengazi?"

31 Iye anayankha kuti, "Ndingamvetse bwanji popanda wina wondima-
sulira?" Ndipo iye anayitana Filipo kuti abwere ndikukhala naye m'galeta.

32 Mawu amene ndunayo imawerenga anali awa:

"Monga mwana wankhosa wopita naye kokamupha amachitira,
kapena monga nkhosa imakhalira duu poyimeta,
momwemonso iye sanatsekule pakamwa pake.

33 Iye ananyozedwa ndipo panalibe chilungamo pa mlandu wake.
Ndipo ndani amene analabadirako za zidzukulu zake
poona kuti iye anachotsedwa m'dziko la anthu amoyo?"

34 Ndunayo inamufunsa Filipo kuti, "Chonde, uzeni, kodi mneneri
akuyankhula za ndani, za iye mwini kapena za munthu wina?"
35 Pamenepo Filipo anayambira pa malemba omwewo kumuwuza za
Uthenga Wabwino wa Yesu.

36 Akuyenda mu msewu anafika pamalo pamene panali madzi ndipo
ndunayo inati, "Taonani madzi awa. Kodi pali chondiletsa kuti ndiba-
tizidwe?" 37 Filipo anati, "Ngati mukhulupirira ndi mtima wanu wonse
mukhoza kubatizidwa." Ndunayo inayankha kuti, "Ine ndikukhulupirira
kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu." 38 Ndipo analamulira galeta
kuti liyime. Onse awiriwo, Filipo ndi Ndunayo anatsika ndi kulowa
m'madzi ndipo Filipo anamubatiza. 39 Pamene iwo anatuluka m'madzimo,
Mzimu wa Ambuye anamukwatula Filipo, ndipo Ndunayo sinamuonenso,
koma inapitiriza ulendo wake ikusangalala. 40 Koma Filipo anapezeka
kuti ali ku Azoto ndipo anazungulira konse, kulalikira Uthenga Wabwino
m'mizinda yonse mpaka anakafika ku Kaisareya.

# 9

### *Kutembenuka Mtima kwa Saulo*

1 Pa nthawi imeneyi, Saulo ankaopsezabe okhulupirira Ambuye nafuna
kuwapha. Iye anapita kwa mkulu wa ansembe, 2 ndi kukapempha
makalata a chilolezo kuti apite nawo ku masunagoge a ku Damasiko, kuti
ngati atakapezeka ena kumeneko otsata Njirayo, kaya ndi amuna kapena
amayi, akawamange ndi kuwatenga kubwera nawo ku Yerusalemu.
3 Akuyandikira ku Damasikoku paulendo wake, mwadzidzidzi kuwala
kochokera kumwamba kunamuzungulira iye. 4 Iye anagwa pansi ndipo
anamva mawu akuti, "Saulo, Saulo ukundizunziranji Ine?"

5 Saulo anafunsa kuti, "Ndinu yani Ambuye?"

Ambuye anayankha kuti, "Ndine Yesu amene iwe ukumuzunza."
6 "Tsopano dzuka, lowa mu mzindamo, ndipo udzawuzidwa zoyenera
kuchita."

7 Anthu amene anali naye paulendo, anasowa chonena; iwo anamva
mawu koma sanaone wina aliyense. 8 Saulo anayimirira, ndipo pamene
anatsekula maso ake sanathe kuona. Kotero anamugwira dzanja ndi
kulowa naye mu Damasiko. 9 Anakhala wosaona kwa masiku atatu
ndiponso sanadye kapena kumwa kanthu kalikonse.

10 Ku Damasiko kunali wophunzira wina dzina lake Hananiya. Ambuye
anamuyitana m'masomphenya kuti, "Hananiya!"

Iye anayankha kuti, "Ine Ambuye."

11 Ambuye anamuwuza iye kuti, "Nyamuka, pita ku nyumba ya Yudasi
imene ili pa Njira Yolunjika ndipo ukafunse za munthu wochokera
ku Tarisisi dzina lake Saulo, pakuti akupemphera. 12 Ndipo waona
m'masomphenya munthu, dzina lake Hananiya atabwera ndi kumusan-
jika manja kuti aonenso."
13 Hananiya anayankha kuti, "Ambuye, ndinamva zambiri za munthu
uyu ndi zonse zoyipa anachitira oyera mtima a ku Yerusalemu. 14 Ndipo
wabwera kuno ndi ulamuliro wa akulu ansembe kuti adzamange onse
amene amayitana pa dzina lanu."
15 Koma Ambuye anati kwa Hananiya, "Pita! Munthu uyu ndi chida
changa chosankhika chonyamulira dzina langa pamaso pa anthu a
mitundu ina ndi mafumu awo ndiponso kwa anthu a Israeli. 16 Ine
ndidzamuonetsa zowawa zonse zimene ayenera kumva chifukwa cha
dzina langa."
17 Pamenepo Hananiya ananyamuka ndi kukalowa m'nyumbayo. Ana-
musanjika manja Sauloyo ndipo anati, "M'bale Saulo, Ambuye Yesu,
amene anakuonekera pa msewu pamene umabwera kuno wandituma
kuti uwonenso ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera." 18 Nthawi yomweyo
m'maso mwa Saulo munachoka zinthu zokhala ngati mamba ansomba,
ndipo anayambanso kuona. Iye anayimirira nabatizidwa, 19 ndipo atadya
chakudya, anapezanso mphamvu.

*Saulo Alalikira ku Damasiko*

Saulo anakhala masiku angapo ndi ophunzira a ku Damasiko.
20 Posakhalitsa anayamba kulalikira m'sunagoge kuti Yesu ndiye Mwana
wa Mulungu. 21 Onse amene anamva iye akulalikira anadabwa ndipo
anafunsa kuti, "Kodi uyu si munthu amene anayambitsa kuzunza
okhulupirira ku mpingo wa ku Yerusalemu? Kodi siwabwera kuno kuti
awamange ndi kuwapereka kwa akulu a ansembe?" 22 Koma mphamvu
za Saulo zinali kukulirakulira ndipo anathetsa nzeru Ayuda okhala ku
Damasiko powatsimikizira kuti Yesu ndi Mpulumutsi.
23 Patapita masiku ambiri, Ayuda anapangana zoti aphe Saulo, 24 koma
iye anadziwa za chiwembucho. Anthu ankadikirira usana ndi usiku pa
zipata za mzindawo kuti amuphe. 25 Koma ophunzira ake anamutenga
usiku, namutsitsira kunja kwa mpandawo m'dengu.

*Saulo ku Yerusalemu*

26 Saulo atafika ku Yerusalemu, anayesetsa kulowa m'gulu la ophunzira
koma onse anamuopa chifukwa sanakhulupirire kuti anali wophunziradi.
27 Koma Barnaba anamutenga napita naye kwa atumwi. Iye anawafo-
tokozera iwo za mmene Saulo anaonera Ambuye pa njira paja, ndi kuti
Ambuye anamuyankhula, ndi momwe analalikira ku Damasiko m'dzina
la Yesu mosaopa. 28 Kotero Saulo anakhala nawo nayendayenda mwau-
fulu mu Yerusalemu akulalikira molimba mtima m'dzina la Ambuye.
29 Anayankhula ndi kutsutsana ndi Ayuda a Chihelene, koma iwo ankafuna
kumupha. 30 Abale atadziwa zimenezi, anamutenga Saulo ndi kupita naye
ku Kaisareya, ndipo anamutumiza ku Tarisisi.
31 Pamenepo mpingo wa ku Yudeya konse, ku Galileya ndi ku Samariya
unakhala pamtendere, unalimbikitsidwa; ndi kupatsidwa mphamvu ndi
Mzimu Woyera, unakula m'chiwerengero, ndi kukhala moopa Ambuye.

*Eneya ndi Tabita*

32 Pamene Petro amayendera mpingo, anapita kukachezera oyera mtima
a ku Luda. 33 Kumeneko anakapeza munthu dzina lake Eneya, wofa
ziwalo amene anagona pa mphasa kwa zaka zisanu ndi zitatu. 34 Petro
anati kwa iye, "Eneya, Yesu Khristu akukuchiritsa iwe, dzuka ndipo yalula
mphasa yako." Nthawi yomweyo Eneya anayimirira. 35 Anthu onse amene
anakhala ku Luda ndi ku Sharoni anamuona ndipo anatembenukira kwa
Ambuye.

36 Ku Yopa kunali wophunzira wina dzina lake Tabita (m'Chigriki amati
Dorika) amene nthawi zonse ankachita zachifundo ndiponso kuthandiza
osauka. 37 Nthawi imeneyi anadwala ndipo anamwalira, anasambitsa
thupi lake, namugoneka m'chipinda chammwamba. 38 Popeza ku Yopa
kunali pafupi ndi Luda; pamene ophunzira anamva kuti Petro anali ku
Luda, anatuma anthu awiri kuti akamudandaulire kuti, "Chonde bwerani
kuno msanga!"

39 Petro ananyamuka, napita nawo, ndipo atafika anamutengera ku
chipinda chammwamba. Amasiye onse anayima momuzungulira akulira
ndi kumuonetsa mwinjiro ndi zovala zina zimene Dorika ankapanga
akanali moyo.

40 Petro anatulutsa anthu onse m'chipindamo; ndipo anagwada pansi
ndi kupemphera. Anatembenukira mtembo uja nati, "Tabita, dzuka,"
Tabita anatsekula maso ake, ndipo ataona Petro anakhala pansi. 41 Petro
anamugwira dzanja, namuyimiritsa. Ndipo anayitana okhulupirira ndi
amasiye namupereka wamoyo. 42 Zimenezi zinadziwika ku Yopa konse,
ndipo anthu ambiri anakhulupirira Ambuye. 43 Petro anakhala ku Yopa
kwa masiku ambiri kwa munthu wina, dzina lake Simoni, mmisiri wa
zikopa.

# 10

### *Kenturiyo Korneliyo Ayitana Petro*

1 Ku Kaisareya kunali munthu wina dzina lake Korneliyo, mkulu wa
asilikali 100 wa gulu la Italiya. 2 Iye ndi banja lake lonse amapembedza
ndi kuopa Mulungu. Iye amathandiza osowa mowolowamanja ndipo
amapemphera kwa Mulungu nthawi zonse. 3 Tsiku lina, nthawi ili ngati 3
koloko masana, anaona masomphenya. Anaona bwino ndithu mngelo wa
Mulungu, amene anabwera kwa iye ndi kuti, "Korneliyo."

4 Korneliyo anamuyang'anitsitsa mngeloyo mwa mantha. Iye anafunsa
kuti, "N'chiyani kodi Ambuye?"

Mngelo anayankha kuti, "Mapemphero ako ndi zachifundo zako zafika
pamaso pa Mulungu ngati chikumbutso. 5 Tsopano tuma anthu apite ku
Yopa kuti akayitane munthu dzina lake Simoni Petro. 6 Iye akukhala ndi
Simoni mmisiri wa zikopa, amene nyumba yake ili m'mbali mwa nyanja."

7 Mngeloyo anayankhula naye anachoka, Korneliyo anayitana antchito
ake awiri ndiponso msilikali mmodzi wa iwo amene ankamutumikira
yemwe ankapembedza Mulungu. 8 Iye anawafotokozera zonse zimene
zinachitika ndipo anawatuma kuti apite ku Yopa.

### *Masomphenya a Petro*

9 Mmawa mwake, nthawi ili ngati 12 koloko anthuwo atayandikira
mzindawo, Petro anakwera pa denga kukapemphera. 10 Iye anamva
njala ndipo anafuna chakudya, ndipo akukonza chakudyacho, iye anachita
ngati wakomoka. 11 Iye anaona kuthambo kutatsekuka, ndi chinthu china

chikutsitsidwa pansi chooneka ngati chinsalu chachikulu chomangidwa
pa msonga zake zinayi. 12 M'menemo munali nyama zonse zamiyendo
inayi pamodzinso ndi zokwawa za dziko lapansi ndiponso mbalame
zamlengalenga. 13 Petro anamva mawu akuti, "Petro, dzuka, ipha nudye."

14 Petro anayankha kuti, "Ayi, Ambuye! Ine sindinadyepo kanthu
kosayeretsedwa kapena konyansa."

15 Petro anamvanso kachiwiri mawu akuti, "Usachiyese chonyansa
chimene Mulungu wachiyeretsa."

16 Zimenezi zinachitika katatu ndipo nthawi yomweyo chinsalu chija
chinatengedwanso kupita kumwamba.

17 Petro akuganizira za tanthauzo la masomphenyawo, anthu amene
Korneliyo anawatuma anapeza kumene kunali nyumba ya Simoni ndipo
anayima pa chipata. 18 Iwo anayitana nafunsa ngati Simoni amene
amadziwika ndi dzina loti Petro amakhala kumeneko.

19 Petro akuganizirabe za masomphenyawo, Mzimu Woyera anati kwa
iye, "Simoni, anthu atatu akukufunafuna. 20 Dzuka, tsika. Usakayike upite
nawo pakuti ndawatuma ndine."

21 Petro anatsika ndipo anati kwa anthuwo, "Amene mukufunayo ndine.
Mwabwera kuno chifukwa chiyani?"

22 Anthuwo anayankha kuti, "Ife tachokera kwa Korneliyo, mkulu
woyang'anira asilikali 100. Iye ndi munthu wolungama ndiponso woopa
Mulungu, amene amalemekezedwa ndi Ayuda onse. Mngelo woyera
anamuwuza kuti mupite ku nyumba yake kuti akamve mawu amene
inu mukanene." 23 Pamenepo Petro anawalowetsa m'nyumba ndipo
anawasamala ngati alendo ake. Mmawa mwake Petro ananyamuka napita
nawo ndipo abale ena a ku Yopa anapita naye pamodzi.

### *Petro ku Nyumba ya Korneliyo*

24 Tsiku linalo Petro anafika ku Kaisareya. Korneliyo anawadikirira
ndipo anali atawasonkhanitsa pamodzi abale ake ndi abwenzi ake a
pamtima. 25 Petro akulowa m'nyumba, Korneliyo anakumana naye ndipo
anadzigwetsa pa mapazi ake namulambira. 26 Koma Petro anamuyimiritsa
nati, "Imirira, inenso ndine munthu ngati iwe."

27 Akuyankhula naye, Petro analowa m'nyumba ndipo anapeza gulu
lalikulu la anthu litasonkhana. 28 Iye anawawuza kuti, "Inu mukudziwa
bwino kuti ndi kutsutsana ndi lamulo ngati Myuda ayanjana ndi Mkunja
kapena kuyendera wina aliyense wa mtundu wina. Koma Mulungu
wandionetsa ine kuti ndisatchule munthu aliyense kuti ndi wosayenera
kapena wonyansa. 29 N'chifukwa chake ndabwera mosawiringula pamene
munandiyitana. Tsopano ndikufunseni," Mwandiyitanira chiyani?

30 Komeliyo anayankha kuti, "Masiku anayi apitawo, nthawi yonga
yomwe ino, 3 koloko masana ndimapemphera m'nyumba mwanga.
Mwadzidzidzi patsogolo panga panayimirira munthu wovala zovala
zonyezimira. 31 Ndipo anati, 'Korneliyo, Mulungu wamva mapemphero
ako ndipo wakumbukira mphatso zako kwa osauka. 32 Tuma anthu
ku Yopa akayitane Simoni wotchedwa Petro. Iye akukhala m'nyumba
ya Simoni mmisiri wazikopa amene amakhala m'mbali mwa nyanja.'
33 N'chifukwa chake ndinatumiza anthu nthawi yomweyo ndipo mwachita
bwino kuti mwabwera. Tsopano ife tonse tili pano pamaso pa Mulungu
kuti timve zonse zimene Ambuye akukulamulani kuti mutiwuze ife."

34 Ndipo Petro anayamba kuyankhula nati, “Zoonadi, tsopano
ndazindikira kuti Mulungu sakondera. 35 Koma amalandira anthu a
mtundu uli wonse amene amaopa Iye ndiponso kuchita chilungamo.
36 Uwu ndi uthenga umene Mulungu anatumiza kwa Aisraeli, kulalikira
Uthenga Wabwino wamtendere mwa Yesu Khristu amene ndi Ambuye
wa onse. 37 Inu mukudziwa zimene zinachitika ku Yudeya konse,
kuyambira ku Galileya pambuyo pa ubatizo umene Yohane analalikira,
38 kuti Mulungu, anamudzoza Yesu, wa ku Nazareti ndi Mzimu Woyera ndi
mphamvu ndiponso mmene Iye anapita nachita zabwino ndi kuchiritsa
onse amene anali pansi pa mphamvu ya mdierekezi, popeza kuti Mulungu
anali naye.

39 “Ife ndife mboni za zonse zimene anachita m’dziko la Ayuda ndiponso
ku Yerusalemu. Anamupha Iye pakumupachika pa mtengo, 40 koma
Mulungu anamuukitsa kwa akufa pa tsiku lachitatu, ndipo analola kuti
aonekere poyera. 41 Iye sanaonekere kwa anthu onse koma kwa mboni
zimene Mulungu anazisankhiratu, kwa ife amene timadya ndi kumwa
naye atauka kwa akufa. 42 Iye anatilamulira ife kuti tilalikire kwa
anthu ndi kuchitira umboni kuti Iye ndiye amene Mulungu anamusankha
kukhala woweruza wa amoyo ndi akufa. 43 Aneneri onse achitira Iye
umboni kuti aliyense amene akhulupirira Iye amakhululukidwa machimo
chifukwa cha dzina lake.”

44 Petro akuyankhulabe mawu amenewa, Mzimu Woyera unatsikira pa
onse amene amamva uthengawo. 45 Abale a mdulidwe omwe anabwera
ndi Petro anadabwa kuona kuti mphatso ya Mzimu Woyera yapatsidwanso
kwa anthu a mitundu ina. 46 Pakuti anamva iwo akuyankhula m’malilime
ndi kuyamika Mulungu. Ndipo Petro anati, 47 “Kodi alipo amene
angawaletse anthu awa kubatizidwa m’madzi? Iwotu alandira Mzimu
Woyera monga ifenso.” 48 Tsono iye analamula kuti abatizidwe m’dzina
la Yesu Khristu. Ndipo anthu aja anamupempha Petro kuti akhale nawo
masiku angapo.

# 11

*Petro Afotokozera Mpingo*

1 Atumwi ndi abale a ku Yudeya konse anamva kuti anthu a mitundu
ina analandiranso Mawu a Mulungu. 2 Tsono Petro atafika ku Yerusalemu,
abale amene anali a mdulidwe anamutsutsa iye, 3 ndipo anati, “Iwe
unalowa m’nyumba ya anthu osachita mdulidwe ndi kudya nawo.”

4 Koma Petro anayamba kuwafotokozera zonse mwatsatanetsatane
momwe zinachitikira kuti, 5 “Ine ndimapemphera mu mzinda wa Yopa
ndipo ndili ngati wokomoka ndinaona masomphenya. Ndinaona chinthu
chokhala ngati chinsalu chachikulu chikutsika kuchokera kumwamba
chogwiriridwa msonga zake zinayi, ndipo chinatsikira pa ine. 6 Ine
ndinayang’ana m’kati mwake ndipo ndinaona nyama za miyendo inayi
za m’dziko lapansi, zirombo, zokwawa, ndi mbalame zamlengalenga.
7 Kenaka ine ndinamva mawu akuti, ‘Petro, Imirira. Ipha, nudye.’

8 “Ine ndinayankha kuti, ‘Ayi, Ambuye! Pakuti chinthu chodetsedwa ndi
chonyansa sindinadyepo pakamwa pangapa.’

9 “Mawu ochokera kumwamba ananenanso kachiwiri kuti, ‘Chimene
Mulungu wachiyeretsa usanene kuti ndi chodetsedwa.’ 10 Zimenezi
zinachitika katatu ndipo kenaka zonse zinatengedwa kupita kumwamba.

11 "Nthawi yomweyo anthu atatu amene anatumidwa kuchokera ku
Kaisareya anayima pa nyumba yomwe ndimakhalayo. 12 Mzimu anandi-
wuza kuti ndisakayike, koma ndipite nawo. Abale asanu ndi mmodzi
awa anapitanso nane ndipo tinalowa m'nyumba ya munthuyo. 13 Iye
anatiwuza mmene anaonera mngelo atayimirira m'nyumba mwake ndi
kumuwuza kuti, 'Tumiza anthu ku Yopa kuti akayitane Simoni wotchedwa
Petro. 14 Iye adzakuwuza uthenga umene udzapulumutsa iwe ndi a pa
banja ako.'

15 "Nditangoyamba kuyankhula, Mzimu Woyera anafika pa iwo monga
momwe anafikira pa ife poyamba paja. 16 Kenaka ndinakumbukira
zimene Ambuye ananena kuti, 'Yohane anabatiza ndi madzi, koma inu
mudzabatizidwa ndi Mzimu Woyera.' 17 Tsono ngati Mulungu anawapatsa
iwo mphatso yomweyo imene anatipatsa ife, amene tinakhulupirira
Ambuye Yesu Khristu, ndine yani kuti nditsutsane ndi Mulungu?"

18 Iwo atamva zimenezi analibenso chonena ndipo anayamika Mulungu
nati, "Potero Mulungu wapatsa anthu a mitundu ina mwayi wotembenuka
mtima ndi kulandira moyo."

### *Mpingo wa ku Antiokeya*

19 Tsopano amene anabalalika chifukwa cha mazunzo amene anayamba
ataphedwa Stefano, anapita mpaka ku Foinike, ku Kupro ndi ku Antiokeya,
ndipo ankalalikira kwa Ayuda okha. 20 Komabe, ena pakati pawo
ochokera ku Kupro ndi ku Kurene anapita ku Antiokeya ndipo iwo
anayamba kuyankhulanso kwa Agriki, nawawuza za Uthenga Wabwino
wa Ambuye Yesu. 21 Mphamvu ya Ambuye inali nawo ndipo anthu ambiri
anakhulupirira natembenukira kwa Ambuye.

22 Mbiri imeneyi inamveka ku mpingo wa ku Yerusalemu ndipo iwo
anatumiza Barnaba ku Antiokeya. 23 Atafika ndi kuona chisomo cha
Mulungu pa iwo, anakondwa ndi kuwalimbikitsa anthu onsewo kuti
apitirire kukhala woona mu mtima mwa Ambuye. 24 Barnabayo anali
munthu wabwino, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi chikhulupiriro
ndipo gulu lalikulu la anthu linabwera kwa Ambuye.

25 Kenaka Barnaba anapita ku Tarisisi kukafuna Saulo, 26 ndipo
pamene anamupeza anabwera naye ku Antiokeya. Barnaba ndi Saulo
anasonkhana ndi mpingo kwa chaka chimodzi naphunzitsa anthu ambir-
imbiri. Okhulupirirawo anayamba kutchedwa Akhristu ku Antiokeya.

27 Masiku amenewo ku Antiokeya kunafika aneneri ena ochokera ku
Yerusalemu. 28 Mmodzi wa iwo dzina lake Agabu, anayimirira ndipo
Mzimu anamutsogolera kunenera zam'tsogolo kuti padzakhala njala
yayikulu pa dziko lonse lapansi. (Izi zinachitikadi nthawi ya ulamuliro
wa Klaudiyo). 29 Ophunzirawo, aliyense monga mwakupata kwake,
anatsimikiza kuthandiza abale okhala ku Yudeya. 30 Izi anazichitadi ndipo
anatuma Barnaba ndi Saulo kukapereka mphatsozo kwa akulu a mpingo.

## 12

### *Petro Apulumuka M'ndende*

1 Inali nthawi yomweyi imene mfumu Herode anamanga ena a mu
mpingo ndi cholinga chakuti awazunze. 2 Iye analamula kuti Yakobo
m'bale wa Yohane, aphedwe ndi lupanga. 3 Ataona kuti zimenezi zi-
nakondweretsa Ayuda, anawonjeza ndi kugwiranso Petro. Izi zinachitika
pa nthawi ya Chikondwerero cha Buledi wopanda Yisiti. 4 Atamugwira

Petro, namutsekera m'ndende, anamupereka kwa magulu anayi a asilikali
kuti amuyang'anire, gulu lililonse linali ndi asilikali anayi. Herode
anafuna kumuzenga mlandu pamaso pa anthu onse chikondwerero cha
Paska chitapita.

5 Kotero Petro anasungidwa m'ndende, koma mpingo unamupempher-
era kolimba kwa Mulungu.

6 Usiku woti mmawa mwake Herode amuzenga mlandu, Petro amagona
pakati pa asilikali awiri, atamangidwa maunyolo awiri, ndiponso alonda
atayima pa khomo. 7 Mwadzidzidzi mngelo wa Ambuye anaonekera
ndipo kuwala kunawunika m'chipindamo. Mngeloyo anamugwedeza
Petro m'nthiti ndi kumudzutsa. Iye anati, "Fulumira, imirira!" Ndipo
maunyolo anagwa kuchoka m'manja a Petro.

8 Kenaka mngelo anati kwa iye, "Vala zovala ndi nsapato." Ndipo Petro
atachita izi mngeloyo anamuwuzanso kuti, "Funda chovala chako ndipo
unditsate." 9 Petro anatsatira natuluka m'ndende, koma sanazindikire kuti
zimene mngeloyo amachita zimachitikadi; iye amaganiza kuti amaona
masomphenya. 10 Iwo anadutsa gulu loyamba ndi lachiwiri la asilikali
ndipo anafika pa chitseko chachitsulo cholowera mu mzinda. Chitsekocho
chinatsekuka chokha ndipo anadutsa. Pamene anayenda kutalika kwa
msewu umodzi, mwadzidzidzi mngelo uja anachoka.

11 Pamenepo Petro anazindikira nati, "Tsopano ndikudziwa mosakayika
kuti Ambuye anatuma mngelo wake kudzandipulumutsa m'manja mwa
Herode, ndi ku zoyipa zonse zimene Ayuda amafuna kundichitira."

12 Atazindikira zimenezi anapita ku nyumba ya Mariya amayi ake
a Yohane, wotchedwanso Marko, kumene kunasonkhana anthu ambiri
ndipo amapemphera. 13 Petro anagogoda pa chitseko cha panja, ndipo
mtsikana wantchito dzina lake Roda anabwera kuti adzatsekule chitseko.
14 Atazindikira mawu a Petro anakondwa kwambiri ndipo anabwerera
osatsekula ndipo anafuwula kuti, "Petro ali pa khomopa!"

15 Anthuwo anati kwa iye, "Wopenga iwe!" Atalimbikira kunena kuti
zinali zoona, iwo anati, "Ameneyo ndi mngelo wake."

16 Koma Petro anapitiriza kugogoda ndipo atatsekula chitseko ndi
kumuona, anthuwo anadabwa kwambiri. 17 Petro anakweza dzanja ndi
kuwawuza kuti akhale chete ndipo anawafotokozera mmene Ambuye
anamutulutsira m'ndende. Iye anati, "Uzani Yakobo ndi abale ena za
zimenezi." Kenaka anachoka napita kumalo ena.

18 Pamene kunacha kunali phokoso lalikulu pakati pa asilikali, iwo
anafunsa kuti, "Kodi chamuchitikira Petro ndi chiyani?" 19 Herode ata-
mufunafuna ndipo wosamupeza, anawafunsa asilikali ndipo analamulira
kuti asilikaliwo aphedwe.

*Imfa ya Herode*

Kenaka Herode anachoka ku Yudeya ndi kupita ku Kaisareya ndipo
anakhala kumeneko kwa kanthawi 20 Herode anakwiyira anthu a ku
Turo ndi Sidoni; anthuwo anagwirizana zoti akambirane naye. Atapeza
thandizo kuchokera kwa Blasito, wantchito wokhulupirika wa mfumu,
anapempha kuti pakhale mtendere, chifukwa dziko lawo limadalira dziko
la mfumuyo pa chakudya chawo.

21 Pa tsiku limene anasankha Herode, atavala zovala zake zaufumu,
anakhala pa mpando wake ndipo anayankhula kwa anthuwo. 22 Anthuwo
anafuwula nati, "Amenewa ndi mawu a mulungu osati a munthu

ayi.” 23 Nthawi yomweyo mngelo wa Mulungu anamukantha chifukwa
sanapereke ulemu kwa Mulungu ndipo anadyedwa ndi mphutsi nafa.
24 Koma Mawu a Mulungu anapitirirabe kufalikirafalikira.
25 Barnaba ndi Saulo atamaliza ntchito yawo anachoka ku Yerusalemu,
atatenga Yohane wotchedwanso Marko.

# 13

*Barnaba ndi Saulo Atumidwa ndi Mpingo*

1 Mu mpingo wa ku Antiokeya munali aneneri ndi aphunzitsi awa:
Barnaba, Simeoni, Lukia wa ku Kurene, Manayeni (amene analeredwa
pamodzi ndi mfumu Herode), ndiponso Saulo. 2 Iwo pamene ankapem-
bedza Ambuye ndi kusala kudya, Mzimu Woyera anati, “Mundipatulire
Barnaba ndi Saulo kuti akagwire ntchito imene ndinawayitanira.” 3 Ndipo
atasala kudya ndi kupemphera anasanjika manja awo pa iwo nawatumiza.

*Ku Kupro*

4 Barnaba ndi Saulo motumidwa ndi Mzimu Woyera, anapita ku
Selukeya ndipo kuchokera kumeneko anakwera sitima ya pamadzi kupita
ku Kupro. 5 Pamene anafika ku Salamisi, analalikira Mawu a Mulungu
m’Masunagoge a Ayuda. Iwo anali ndi Yohane monga wowatumikira.
6 Iwo anayenda pa chilumba chonse mpaka anafika ku Pafo, kumeneko
anapezanako ndi Myuda, wamatsenga amene analinso mneneri wonama
dzina lake Barayesu. 7 Iyeyu, amathandiza mkulu wa boma, Sergio
Paulo. Mkulu wa bomayu, munthu wanzeru, anayitana Barnaba ndi
Saulo chifukwa anafuna kumva Mawu a Mulungu. 8 Koma Elima
wamatsengayo, (Elima tanthauzo lake ndi wamatsenga), anatsutsana
nawo ndipo anafuna kumuletsa mkulu wa bomayo kuti asakhulupirire.
9 Koma Saulo, amenenso amatchedwa Paulo, wodzazidwa ndi Mzimu
Woyera anamuyang’anitsitsa Elima ndipo anati, 10 “Iwe ndiwe mwana
wa mdierekezi ndiponso mdani wa chilungamo! Ndiwe wodzaza ndi
chinyengo cha mtundu uliwonse ndi kuchenjera konse. Kodi sudzaleka
kupotoza njira zolungama za Ambuye? 11 Tsopano dzanja la Ambuye
likukutsutsa iwe. Udzakhala wosaona ndipo kwa kanthawi sudzatha
kuona kuwala kwa dzuwa.”
Nthawi yomweyo khungu ndi mdima zinamugwera ndipo anafunafuna
munthu woti amugwire dzanja kuti amutsogolere. 12 Pamene mkulu wa
bomayo anaona zimene zinachitika anakhulupirira pakuti anadabwa ndi
chiphunzitso cha Ambuye.

*Antiokeya wa ku Pisidiya*

13 Kuchokera ku Pafo, Paulo ndi anzake anayenda pa sitima ya pamadzi
kupita ku Perga wa ku Pamfiliya, kumeneko Yohane anawasiya nabwerera
ku Yerusalemu. 14 Kuchokera ku Perga anapita ku Pisidiya wa ku
Antiokeya. Pa tsiku la Sabata analowa m’sunagoge, nakhala pansi.
15 Atawerenga mawu a m’Malamulo ndi Aneneri, akulu a sunagoge
anawatumizira mawu ndi kuti, “Abale ngati muli ndi mawu olimbikitsa
nawo anthuwa, nenani.”
16 Atayimirira, Paulo anakweza dzanja lake ndi kuti, “Inu Ais-
raeli ndiponso inu a mitundu ina amene mumapembedza Mulungu,
tandimverani! 17 Mulungu wa Aisraeli anasankha makolo athu ndipo
anawapatsa chuma chambiri pamene amakhala ku Igupto. Anawatulutsa
m’dzikomo ndi dzanja lake lamphamvu. 18 Ndipo Iye anapirira khalidwe

lawo m’chipululu kwa zaka makumi anayi. [19] Mulungu anawagonjetsera
mitundu isanu ndi iwiri ya ku Kanaani ndipo anapereka dzikolo kwa
Israeli kuti likhale lawo. [20] Izi zonse zinatenga zaka 450.
“Zitatha izi, Mulungu anawapatsa oweruza mpaka nthawi ya mneneri
Samueli. [21] Kenaka anthu anapempha kuti awapatse mfumu, ndipo
anawapatsa Sauli mwana wa Kisi, wa fuko la Benjamini amene anala-
mulira zaka makumi anayi. [22] Mulungu atamuchotsa Sauli, anayika
Davide kukhala mfumu yawo. Mulungu anamuchitira umboni kuti,
‘Ndapeza Davide mwana wa Yese munthu wa pamtima panga; iye
adzachita zonse zimene ine ndikufuna kuti iye achite.’

[23] “Kuchokera mwa zidzukulu za munthu ameneyu, Mulungu anawutsa
Yesu kukhala Mpulumutsi wa Aisraeli, monga analonjezera. [24] Yesu
asanabwere, Yohane analalikira kwa anthu onse Aisraeli za kutembenuka
mtima ndi ubatizo. [25] Pamene Yohane amatsiriza ntchito yake anati:
‘Mukuganiza kuti ine ndine yani? Ine sindine ameneyo ayi, koma Iye
akubwera pambuyo panga, amene ine sindine woyenera kumasula zingwe
za nsapato zake.’

[26] “Abale, ana a Abrahamu, ndiponso inu a mitundu ina amene
mumaopa Mulungu, Iye watumiza uthenga wachipulumutsowo kwa
ife. [27] Anthu a ku Yerusalemu ndi atsogoleri awo sanazindikire Yesu,
komabe pomuweruza Yesu anakwaniritsa mawu a Aneneri amene amaw-
erengedwa Sabata lililonse. [28] Ngakhale sanapeze chifukwa choti afe,
anapempha Pilato kuti amuphe. [29] Atachita zonse zimene zinalembedwa
za Iye, iwo anamuchotsa pa mtengo ndipo anamuyika m’manda. [30] Koma
Mulungu anamuukitsa, [31] ndipo kwa masiku ambiri anaonekera kwa
amene anayenda naye kuchokera ku Galileya mpaka ku Yerusalemu.
Iwowa tsopano ndi mboni zake kwa anthu a Israeli.

[32] “Ife tikukuwuzani Uthenga Wabwino; umene Mulungu analonjeza
makolo athu. [33] Iye wakwaniritsa zimenezi kwa ife ana awo, poukitsa
Yesu kuchokera kwa akufa. Monga zinalembedwa mu Salimo lachiwiri
kuti,

“Iwe ndiwe mwana wanga;
lero ine ndakhala Atate ako.”

[34] Zakuti Mulungu anamuukitsa kuti asawole konse, zinanenedwa
m’mawu awa:

“ ‘Ine, ndidzakupatsa madalitso opatulika ndi odalirika amene ndinalon-
jeza Davide.’

[35] N’chifukwa chakenso zinalembedwa mu Salimo lina kuti,

“ ‘Simudzalekerera woyera wanu kuti awole.’

[36] “Pakuti pamene Davide anatsiriza kutumikira Mulungu mu m’bado
wake, anamwalira, iye anayikidwa m’manda pamodzi ndi makolo ake
ndipo thupi lake linawola. [37] Koma amene Mulungu anamuukitsa kwa
akufa sanawole ayi.

[38] “N’chifukwa chake, abale anga, dziwani kuti mwa Yesu chikhu-
lulukiro cha machimo chikulalikidwa. [39] Kudzera mwa Iye aliyense
amene akhulupirira, alungamitsidwa kuchoka ku tchimo lililonse limene
silingachoke ndi Malamulo a Mose. [40] Samalani kuti zimene aneneri
akunena zisakuchitikireni inu:

[41] “ ‘Onani, inu anthu onyoza,
dabwani ndipo wonongekani,
chifukwa ine ndidzachita china chake m’masiku anu,

inu simudzazikhulupirira
ngakhale wina atakufotokozerani!' "
42 Pamene Paulo ndi Barnaba amatuluka m'Sunagoge, anthu anawapem-
pha kuti adzapitirize kuyankhula zinthu zimenezi Sabata linalo. 43 Atatha
mapemphero, Ayuda ambiri ndi anthu odzipereka otembenukira ku
Chiyuda anatsatira Paulo ndi Barnaba, iwo anayankhula ndi anthuwo
ndipo anawapempha kuti apitirire m'chisomo cha Mulungu.
44 Pa Sabata linalo pafupifupi anthu onse a mu mzindawo anasonkhana
kudzamva Mawu a Ambuye. 45 Pamene Ayuda anaona gulu la anthu,
anachita nsanje ndipo anayankhula zamwano kutsutsana ndi zimene
Paulo amanena.
46 Ndipo Paulo ndi Barnaba anawayankha molimba mtima kuti, "Ife
tinayenera kuyankhula Mawu a Mulungu kwa inu poyamba. Popeza inu
mwawakana ndi kudziyesa nokha osayenera moyo wosatha, ife tsopano
tikupita kwa anthu a mitundu ina. 47 Pakuti izi ndi zimene Ambuye
anatilamula ife:
" 'Ine ndakuyika iwe ukhale kuwunika kwa anthu a mitundu ina,
kuti ukafikitse chipulumutso ku malekezero a dziko lapansi!' "
48 Anthu a mitundu ina atamva izi, anakondwa ndipo analemekeza
Mawu Ambuye; ndipo onse amene anawasankha kuti alandire moyo
osatha anakhulupirira.
49 Mawu a Ambuye anafalikira m'chigawo chonse. 50 Koma Ayuda
anawutsa mitima ya akazi otchuka opembedza Mulungu ndi akulu a mu
mzindamo. Iwo anabweretsa mazunzo kwa Paulo ndi Barnaba ndipo
anawathamangitsa m'chigawo chawo. 51 Tsono iwo anasasa fumbi la ku
mapazi awo powatsutsa, ndipo anapita ku Ikoniya. 52 Ndipo ophunzira
anadzazidwa ndi chimwemwe ndiponso ndi Mzimu Woyera.

# 14

*Ku Ikoniya*

1 Ku Ikoniya, Paulo ndi Barnaba analowanso m'sunagoge ya Ayuda.
Kumeneko iwo anaphunzitsa momveka bwino kotero kuti anthu ambiri
Achiyuda ndi anthu a mitundu ina anakhulupirira. 2 Koma Ayuda
amene anakana kukhulupirira anawutsa anthu a mitundu ina nawononga
maganizo awo kutsutsana ndi abale. 3 Ndipo Paulo ndi Barnaba anakhala
kumeneko nthawi yayitali, nalalikira molimba mtima za Ambuye amene
anawapatsa mphamvu yochitira zozizwitsa ndi zizindikiro zodabwitsa
pochitira umboni mawu a chisomo. 4 Anthu a mu mzindamo ana-
gawikana; ena anali mbali ya Ayuda, ena mbali ya atumwi. 5 Pamenepo
anthu a mitundu ina ndi Ayuda, pamodzi ndi atsogoleri awo anakonza
chiwembu choti azunze atumwiwo ndi kuwagenda ndi miyala. 6 Koma
atazindikira zimenezi, anathawira ku Lusitra ndi Derbe, mizinda ya
ku Lukaoniya, ndiponso ku dziko lozungulira mizindayo, 7 kumene
anapitiriza kulalikira Uthenga Wabwino.

*Ku Lusitra ndi ku Derbe*

8 Ku Lusitra kunali munthu wolumala miyendo, amene sanayendepo
chibadwire chake. 9 Iyeyu, amamvetsera pamene Paulo amayankhula.
Paulo anamuyang'anitsitsa ndipo anaona kuti anali ndi chikhulupiriro
choti achiritsidwe nacho. 10 Ndipo Paulo anamuyitana mofuwula nati,
"Imirira!" Atamva zimenezi, munthuyo anayimirira, nayamba kuyenda.

[11] Gulu la anthu litaona zimene Paulo anachitazi, linafuwula
m'Chilukaoniya kuti, "Milungu yatitsikira yooneka ngati anthu!"
[12] Barnaba anamutcha Zeusi ndipo Paulo anamutcha Herimesi chifukwa
ndiye amatsogolera kuyankhula. [13] Wansembe wa Zeusi amene nyumba
yopembedzera Zeusiyo inali kunja pafupi ndi mzindawo, anabweretsa ng'ombe yayimuna yovekedwa nkhata za maluwa pa chipata cha mzindawo chifukwa iyeyo pamodzi ndi anthu ena onse aja amafuna kudzipereka nsembe kwa Paulo ndi Barnaba.
[14] Koma Barnaba ndi Paulo atamva zimenezi, anang'amba zovala zawo,
nathamangira pakati pa gulu la anthuwo, akufuwula kuti, [15] "Anthu inu,
bwanji mukuchita zimenezi? Ifenso ndife anthu monga inu nomwe. Ife takubweretserani Uthenga Wabwino, kuti musiye zinthu zachabezi ndi kutsata Mulungu wamoyo, amene analenga kumwamba ndi dziko
lapansi, nyanja ndi zonse zimene zili m'menemo. [16] Kale Iye analola
anthu a mitundu ina yonse kutsata njira zawozawo. [17] Komabe wakhala
akudzichitira yekha umboni: Iye amaonetsa kukoma mtima kwake pogwetsa mvula kuchokera kumwamba ndi zipatso pa nyengo yake. Amakupatsani chakudya chambiri ndipo amadzaza mitima yanu ndi
chimwemwe." [18] Ngakhale ndi mawu awa, anavutika kuletsa gulu la anthu
kuti asapereke nsembe kwa iwo.
[19] Kenaka kunabwera Ayuda ena kuchokera ku Antiokeya ndi Ikoniya
nakopa gulu la anthu lija. Iwo anamugenda miyala Paulo namukokera
kunja kwa mzindawo, kuganiza kuti wafa. [20] Koma ophunzira atamuzun-
gulira, Pauloyo anayimirira nalowanso mu mzindawo. Mmawa mwake iye ndi Barnaba anachoka ndi kupita ku Derbe.

### *Paulo ndi Barnaba Abwerera ku Antiokeya wa ku Siriya*

[21] Iwo analalikira Uthenga Wabwino mu mzindawo ndipo anthu ambiri
anatembenuka mtima ndi kukhala ophunzira. Kenaka anabwerera
ku Lusitra, ku Ikoniya ndi ku Antiokeya. [22] Kumeneko analimbikitsa
mitima ya ophunzira ndi kuwapatsa mphamvu kuti akhalebe woona m'chikhulupiriro. Iwo anati, "Ife tiyenera kudutsa m'masautso ambiri
kuti tikalowe mu ufumu wa Mulungu." [23] Paulo ndi Barnaba anasankha
akulu ampingo pa mpingo uliwonse, ndipo atapemphera ndi kusala
kudya anawapereka kwa Ambuye amene anamukhulupirira. [24] Atadutsa
Pisidiya, anafika ku Pamfiliya. [25] Atalalikira Mawu ku Perga, anapita ku
Ataliya.
[26] Ku Ataliyako, anakwera sitima ya pamadzi kubwerera ku Antiokeya
kumene anayitanidwa mwachisomo cha Mulungu kuti agwire ntchito
imene tsopano anali atayitsiriza. [27] Atangofika ku Antiokeya, anasonkhan-
itsa pamodzi mpingo ndipo anafotokoza zonse zimene Mulungu anachita kudzera mwa iwo ndiponso mmene Iye anatsekulira a mitundu ina njira
ya chikhulupiriro. [28] Ndipo anakhala kumeneko ndi ophunzira nthawi
yayitali.

## 15

### *Msonkhano wa ku Yerusalemu*

[1] Anthu ena ochokera ku Yudeya anafika ku Antiokeya ndipo amaphun-
zitsa abale kuti, "Ngati simuchita mdulidwe potsata mwambo wa Mose,
simungapulumuke." [2] Zimenezi zinachititsa Paulo ndi Barnaba kuti atsut-
sane nawo kwambiri. Kotero Paulo ndi Barnaba anasankhidwa pamodzi

ndi abale ena kuti apite ku Yerusalemu kukaonana ndi atumwi ndi akulu
ampingo kukakambirana za nkhaniyi. 3 Mpingo unawaperekeza, ndipo
pamene amadutsa ku Foinike ndi Samariya, iwo anafotokoza momwe a
mitundu ina anatembenukira mtima. Nkhani imeneyi inakondweretsa
kwambiri abale onse. 4 Atafika ku Yerusalemu, iwo analandiridwa ndi
mpingo, pamodzi ndi atumwi ndiponso akulu ampingo. Paulo ndi Barnaba
anawafotokozera zonse zimene Mulungu anachita kudzera mwa iwo.

5 Kenaka, okhulupirira ena amene kale anali a gulu la Afarisi anayimirira ndipo anati, "Anthu a mitundu ina ayenera kuchita mdulidwe ndi kusunga malamulo a Mose."

6 Atumwi ndi akulu ampingo anasonkhana kuti akambirane za nkhaniyi.
7 Atakambirana kwambiri Petro anayimirira, ndipo anawayankhula nati:
"Abale, mukudziwa kuti masiku oyambirira Mulungu anandisankha
ine pakati panu kuti anthu a mitundu ina amve kuchokera pakamwa
panga mawu a Uthenga Wabwino ndi kukhulupirira. 8 Mulungu amene
amadziwa mtima wa munthu, Iye anaonetsa kuti anawalandira powapatsa
Mzimu Woyera, monga momwe anachita kwa ife. 9 Iye sanasiyanitse
pakati pa ife ndi iwo, pakuti anayeretsa mitima yawo mwachikhulupiriro.
10 Tsopano, chifukwa chiyani mukuyesa Mulungu poyika goli m'khosi la
ophunzira, limene ngakhale ife kapena makolo athu sangathe kulisenza?
11 Osatero! Ife tikukhulupirira kuti tinapulumutsidwa mwachisomo cha
Ambuye athu Yesu Khristu, monga iwonso anachitira."

12 Gulu lonse linakhala chete pamene amamvetsera Barnaba ndi Paulo
akuwawuza za zizindikiro zodabwitsa zimene Mulungu anazichita pakati
pa anthu a mitundu ina kudzera mwa iwo. 13 Iwo atatha kuyankhula,
Yakobo anayankhula nati: "Abale, tandimverani. 14 Simoni watifotokozera
mmene Mulungu poyamba paja anaonetsa kukhudzidwa kwake pomwe
anatenga anthu a mitundu ina kukhala ake. 15 Mawu a aneneri
akuvomereza zimenezi, monga kwalembedwa kuti,

16 " 'Zitatha izi Ine ndidzabwerera
ndipo ndidzamanganso nyumba ya Davide imene inagwa.
Ndidzakonzanso malo amene anagumuka,
ndi kuyimanganso,
17 kuti anthu otsalawo afunefune Ambuye,
ndi anthu onse a mitundu ina amene atchedwa ndi dzina langa,
akutero Ambuye, amene amachita zinthu zimenezi
18 zinaululidwa kuyambira kalekale.'

19 "Chifukwa chake, ine ndikuweruza kuti tisamavute anthu a mitundu
ina amene atembenuka mtima kutsata Mulungu. 20 Koma tiwalembere
iwo, kuwawuza kuti asadye chakudya choperekedwa kwa mafano,
apewenso dama, asadyenso nyama zochita kupotola kapena kudya
magazi. 21 Pakuti malamulo a Mose akhala akulalikidwa mu mzinda
uliwonse, kuyambira kalekale ndipo amawerengedwa m'Masunagoge
tsiku la Sabata."

### *Kalata Yopita kwa Anthu a Mitundu ina*

22 Pamenepo atumwi ndi akulu ampingo, pamodzi ndi mpingo onse,
anagwirizana zosankha anthu ena pakati pawo kuti awatume ku Antiokeya pamodzi ndi Paulo ndi Bamaba. Iwo anasankha Yudasi,
wotchedwa Barsaba ndi Sila, anthu awiri amene anali atsogoleri pakati
pa abale, 23 kuti akapereke kalata yonena kuti,

Kuchokera kwa atumwi ndi akulu ampingo, abale anu,

Kwa anthu a mitundu ina okhulupirira a ku Antiokeya, Siriya ndi Kilikiya:
Tikupereka moni.

24 Ife tamva kuti anthu ena ochokera pakati pathu, amene siti-
nawatume anakusokonezani maganizo ndi kukuvutitsani ndi zimene
amakuwuzani. 25 Tsono ife tagwirizana kuti, tisankhe anthu ena ndi
kuwatumiza kwa inu pamodzi ndi abale athu okondedwa Paulo ndi
Barnaba, 26 anthu amene anapereka moyo wawo chifukwa cha dzina
la Ambuye athu Yesu Khristu. 27 N'chifukwa chake, tikutumiza Yudasi
ndi Sila kuti adzachitire umboni ndi mawu a pakamwa pawo za zimene
ife talemba. 28 Pakuti zinakomera Mzimu Woyera ndiponso ife kuti
tisakusenzetseni katundu wina, kupatula zoyenera zokhazi: 29 Mupewe
kudya chakudya choperekedwa nsembe kwa mafano, musadye magazi,
kapena nyama yopha mopotola ndiponso musachite dama. Mudzachita
bwino mukapewa zimenezi.

Tsalani bwino.
30 Anthu aja anatumidwa ndipo anafika ku Antiokeya, kumene ana-
sonkhanitsa mpingo pamodzi napereka kalatayo. 31 Anthuwo anaw-
erenga kalatayo ndipo abalewo anakondwa chifukwa cha mawu ake
achirimbikitso. 32 Yudasi ndi Sila amene analinso aneneri, ananena
zambiri zowalimbikitsa ndi kuwapatsa mphamvu abalewo. 33 Atakhala
kumeneko kwa kanthawi, abale aja anatsanzikana nawo mwamtendere
kuti abwerere kwa amene anawatuma. 34 Koma Sila anasankha kuti
akhale komweko. 35 Koma Paulo ndi Barnaba anatsalira ku Antiokeya
kumene iwo pamodzi ndi ena ambiri anaphunzitsa ndi kulalikira Mawu
a Ambuye.

### *Paulo Asiyana ndi Barnaba*

36 Patapita masiku ena Paulo anati kwa Barnaba, "Tiyeni tibwerere
kuti tikaone abale ku mizinda yonse imene tinalalika Mawu a Ambuye
ndipo tikaone mmene akuchitira." 37 Barnaba anafuna kutenga Yohane,
wotchedwanso Marko, kuti apite nawo. 38 Koma Paulo anaganiza kuti
sichinali cha nzeru kumutenga Yohane chifukwa iye anawathawa ku Pam-
filiya ndipo sanapitirire nawo pa ntchito. 39 Iwo anatsutsana kwambiri
kotero kuti anapatukana. Barnaba anatenga Marko ndipo anakwera
sitima ya pamadzi kupita ku Kupro. 40 Paulo anasankha Sila. Abale
atawapempherera kwa Ambuye kuti alandire chisomo, ananyamuka.
41 Iye anadutsa ku Siriya ndi ku Kilikiya kupita akulimbikitsa mipingo.

## 16

### *Timoteyo Atsagana ndi Paulo ndi Sila*

1 Paulo anafika ku Derbe ndi Lusitra, kumene kumakhala ophunzira
wina dzina lake Timoteyo. Amayi ake anali Myuda wokhulupirira, koma
abambo ake anali Mgriki. 2 Abale a ku Lusitra ndi Ikoniya anamuchitira
iye umboni wabwino. 3 Paulo anafuna kumutenga pa ulendo, kotero
anachita mdulidwe chifukwa cha Ayuda amene amakhala m'deralo pakuti
onse amadziwa kuti abambo ake anali Mgriki. 4 Pamene amayenda
mzinda ndi mzinda, amafotokoza zimene atumwi ndi akulu ampingo
ku Yerusalemu anagwirizana kuti anthu azitsatire. 5 Kotero mipingo

inalimbikitsidwa m'chikhulupiriro ndipo anthu amachulukirachulukirabe tsiku ndi tsiku.

### *Paulo Awona Masomphenya*

6 Paulo ndi anzake anadutsa mayiko a Frugiya ndi Galatiya, Mzimu
Woyera atawaletsa kulalikira Mawu a Mulungu ku Asiya. 7 Atafika ku
malire a Musiya, anayesa kulowa ku Bituniya, koma Mzimu wa Yesu
sunawalole kutero. 8 Ndipo iwo anadutsa Musiya ndipo anapita ku
Trowa. 9 Nthawi ya usiku Paulo anaona masomphenya, munthu wa ku
Makedoniya atayimirira ndi kumupempha kuti, "Bwerani ku Makedoniya,
mudzatithandize." 10 Paulo ataona masomphenyawa, tinakonzeka kupita
ku Makedoniya, kutsimikiza kuti Mulungu anatiyitana kuti tikalalikire
Uthenga Wabwino.

### *Lidia Atembenuka Mtima ku Filipi*

11 Kuchokera ku Trowa tinakwera sitima ya pamadzi kupita ku Samo-
trake ndipo mmawa mwake tinapitirira mpaka ku Neapoli. 12 Kuchokera
kumeneko tinapita ku Filipi, boma la Aroma ndiponso mzinda waukulu
wa dera la Makedoniya. Tinakhala kumeneko masiku owerengeka.
13 Pa tsiku la Sabata tinatuluka mu mzindawo kupita ku mtsinje
kumene timayembekezera kukapeza malo opempherera. Tinakhala pansi
ndipo tinayamba kuyankhula ndi amayi amene anasonkhana pamenepo.
14 Mmodzi wa amayi amene amamvetserawo ndi Lidiya amene amagulitsa
nsalu zofiira, wochokera ku mzinda wa Tiyatira, ndipo amapembedza
Mulungu. Ambuye anatsekula mtima wake kuti amve mawu a Paulo. 15 Iye
ndi a m'banja lake atabatizidwa, anatiyitana kuti tipite ku nyumba yake.
Iye anati, "Ngati mwanditenga ine kukhala wokhulupirira mwa Ambuye,
bwerani mudzakhale m'nyumba mwanga." Ndipo anatiwumiriza ife
kwambiri.

### *Paulo ndi Sila M'ndende*

16 Tsiku lina pamene timapita kumalo wopempherera, tinakumana
ndi mtsikana wina amene anali ndi mzimu woyipa umene umanena
zam'tsogolo. Iye amapezera ndalama zambiri ambuye ake pa ulosi
wake. 17 Mtsikanayu anatsatira Paulo ndi ife, akufuwula kuti, "Anthu
awa ndi atumiki a Mulungu Wammwambamwamba, amene akukuwuzani
inu njira yachipulumutso." 18 Iye anachita izi masiku ambiri. Kenaka
Paulo anavutika mu mtima, natembenuka ndipo anati kwa mzimuwo,
"Ndikukulamula iwe m'dzina la Yesu Khristu kuti utuluke mwa iye!"
Nthawi yomweyo mzimuwo unatuluka.
19 Pamene ambuye a mtsikana uja anazindikira kuti chiyembekezo
chawo chopezera ndalama chatha, anagwira Paulo ndi Sila nawakokera
ku bwalo la akulu. 20 Anawabweretsa iwo kwa oweruza milandu ndipo
anati, "Anthu awa ndi Ayuda, iwo akuvutitsa mu mzinda wathu. 21 Ndipo
akuphunzitsa miyambo imene ife Aroma sitiloledwa kuyilandira kapena
kuyichita."
22 Gulu la anthu linatsutsana ndi Paulo ndi Sila, ndipo woweruza
milandu analamula kuti avulidwe ndi kumenyedwa. 23 Atawakwapula
kwambiri anawaponya m'ndende, nalamula woyang'anira kuti awa-
sunge mosamalitsa. 24 Chifukwa cha mawu amenewa woyang'anira
ndende anakawayika m'chipinda cham'kati mwa ndende, nawamangirira
miyendo yawo m'zigologolo.

25 Koma pakati pa usiku Paulo ndi Sila ankapemphera ndi kuy-
imba nyimbo zolemekeza Mulungu, ndipo akayidi ena ankamvet-
sera. 26 Mwadzidzidzi kunachitika chivomerezi champhamvu kotero
kuti maziko a ndende anagwedezeka. Nthawi yomweyo zitseko
zonse za ndende zinatsekuka, ndipo maunyolo a aliyense anamasuka.
27 Woyang'anira ndende uja atadzuka ku tulo, anaona kuti zitseko za
ndende zinali zotsekula, ndipo anasolola lupanga lake nafuna kudzipha
chifukwa ankaganiza kuti am'ndende athawa. 28 Koma Paulo anafuwula
kuti, "Usadzipweteke! Tonse tilipo!"
29 Woyang'anira ndendeyo anayitanitsa nyale, nathamangira m'kati
ndipo anadzigwetsa pa mapazi a Paulo ndi Sila akunjenjemera. 30 Iye
anawatulutsa kunja ndipo anawafunsa kuti, "Amuna inu, ndichite chiyani
kuti ndipulumuke?"
31 Iwo anayankha kuti, "Khulupirira Ambuye Yesu ndipo udzapulumuka,
iwe ndi a m'banja lako." 32 Kenaka analalikira mawu a Ambuye kwa
iyeyo ndi onse amene anali m'nyumba mwake. 33 Usiku womwewo
woyang'anira ndendeyo anawatenga nakawatsuka mabala awo; ndipo
pomwepo iye ndi a m'banja lake anabatizidwa. 34 Woyang'anira ndendeyo
anapita nawo ku nyumba yake, nakawapatsa chakudya, ndipo banja lonse
linadzazidwa ndi chimwemwe chifukwa anakhulupirira Mulungu.
35 Kutacha, woweruza milandu uja anatuma asilikali kwa woyang'anira
ndendeyo kukanena kuti, "Amasuleni anthu aja." 36 Woyang'anira
ndendeyo anawuza Paulo kuti, "Woweruza milandu walamula kuti iwe
ndi Sila mumasulidwe. Tsopano muzipita. Pitani mumtendere."
37 Koma Paulo anati kwa asilikaliwo: "Iwo anatikwapula pa gulu la
anthu asanatiweruze, ngakhale kuti ndife nzika za Chiroma natiponya
m'ndende. Kodi tsopano akufuna kutitulutsa mwamseri? Ayi! Asiyeni
abwere okha kuti adzatitulutse."
38 Asilikali aja anakafotokozera woweruza milandu ndipo pamene
anamva kuti Paulo ndi Sila anali nzika za Chiroma, anachita mantha. 39 Iye
anabwera kudzawapepesa ndipo anawatulutsa m'ndende, nawapempha
kuti achoke mu mzindawo. 40 Paulo ndi Sila atatuluka m'ndende, anapita
ku nyumba ya Lidiya, kumene anakumana ndi abale nawalimbikitsa.
Kenaka anachoka.

# 17

*Paulo ku Tesalonika*

1 Atadutsa ku Amfipoli ndi Apoloniya, anafika ku Tesalonika, kumene
kunali sunagoge ya Ayuda. 2 Paulo, monga mwachizolowezi chake,
analowa m'sunagoge, ndipo anakambirana nawo Mawu a Mulungu
kwa masabata atatu, 3 kuwafotokozera ndi kuwatsimikizira kuti Khristu
anayenera kufa ndi kuuka. Iye anati, "Yesu amene ndikukulalikirani ndiye
Khristu." 4 Ena mwa Ayuda anakopeka mtima ndipo anatsatira Paulo ndi
Sila, monganso linachitira gulu lalikulu la Agriki woopa Mulungu, pamodzi
ndi amayi odziwika ambiri.
5 Koma Ayuda ena anachita nsanje; kotero anasonkhanitsa anthu
akhalidwe loyipa ochokera pa msika ndipo napanga gulu nayambitsa
chipolowe mu mzindawo. Anathamangira ku nyumba ya Yasoni kukafuna
Paulo ndi Sila kuti awabweretse pa gulu la anthu. 6 Koma atalephera
kuwapeza, anakokera Yasoniyo ndi abale ena ku bwalo la akulu a
mzindawo akufuwula kuti, "Anthu awa, Paulo ndi Sila, amene akhala

akusokoneza dziko lonse lapansi, tsopano afikanso kuno. 7 Yasoni
ndiye anawalandira m'nyumba mwake. Onsewa akuchita zotsutsana ndi
malamulo a Kaisara pomanena kuti palinso mfumu ina, yotchedwa Yesu."
8 Atamva zimenezi, gulu la anthu ndi akulu a mzinda anavutika mu mtima.
9 Iwo analipiritsa Yasoni ndi anzakewo ndipo anawamasula.

### *Ku Bereya*

10 Mdima utagwa, abale anatumiza Paulo ndi Sila ku Bereya. Atafika
kumeneko anapita ku sunagoge ya Ayuda. 11 Tsopano anthu a ku Bereya
anali akhalidwe labwino kusiyana ndi Atesalonika, pakuti iwo analandira
mawu ndi chidwi chachikulu ndipo ankasanthula Malemba tsiku ndi tsiku
kuti aone ngati zimene ankanena Paulozo zinali zoona. 12 Ayuda ambiri
anakhulupirira, monga anachitiranso amayi ndi amuna ambiri odziwika
a Chigriki.
13 Ayuda a ku Tesalonika atadziwa kuti Paulo akulalikira Mawu a
Mulungu ku Bereya, anapitanso kumeneko, ndi kuwutsa mitima ya anthu
nayambitsa chisokonezo. 14 Nthawi yomweyo abale anatumiza Paulo ku
nyanja koma Sila ndi Timoteyo anatsalira ku Bereya. 15 Anthu amene
anamuperekeza Paulo nafika naye ku Atene, ndipo anabwerera ku Bereya
atawuzidwa kuti Sila ndi Timoteyo amutsatire msanga.

### *Ku Atene*

16 Paulo akudikira Timoteyo ndi Sila ku Atene, anavutika mu mtima
kwambiri poona kuti mzindawo unali odzaza ndi mafano. 17 Tsono
anakambirana ndi Ayuda ndi Agriki amene amaopa Mulungu m'sunagoge,
komanso anthu amene amapezeka pa msika tsiku ndi tsiku ndi ena
amene amakumana nawo. 18 Gulu la Aepikureya ndi Astoiki, anthu
anzeru, anayamba kutsutsana naye. Ena a iwo anafunsa kuti, "Kodi
wolongololayu akufuna kunena chiyani?" Enanso anati, "Akuoneka
ngati akulalikira milungu yachilendo." Iwo ananena zimenezi chifukwa
Paulo amalalikira Uthenga Wabwino wa Yesu ndi kuuka kwa akufa.
19 Kenaka iwo anamutenga nafika naye ku bwalo la Areopagi kumene
anamufunsa kuti, "Kodi tingadziweko chiphunzitso chatsopano chimene
ukuchifotokozachi? 20 Iwe ukubweretsa zinthu zina zachilendo m'makutu
mwathu, ndipo ife tikufuna tidziwe tanthauzo lake." 21 Atene onse
ndi alendo amene amakhala kumeneko samachita kanthu kena koma
kufotokoza ndi kumvera fundo zatsopano.
22 Paulo anayimirira m'bwalo la Areopagi nati: "Inu anthu a ku
Atene! Ine ndikuona kuti m'njira zonse ndinu opembedza kwambiri.
23 Pakuti pamene ndimayenda ndi kuona zinthu zimene mumazipem-
bedza, ndapezanso guwa lansembe lolembedwapo kuti, KWA MULUNGU
WOSADZIWIKA. Tsopano chimene mumachipembedza osachidziwa ndi
chimene ndikuchilalikira.
24 "Mulungu amene analenga dziko lapansi ndiponso zonse zili
m'menemo ndiye Ambuye wakumwamba ndi dziko lapansi ndipo sakhala
m'nyumba zachipembedzo zomangidwa ndi manja. 25 Ndipo satu-
mikiridwa ndi manja a anthu ngati kuti Iye amasowa kanthu, chifukwa
Iye ndiye amapereka moyo ndi mpweya kwa anthu onse ndi zina zonse.
26 Kuchoka kwa munthu mmodzi Iye analenga mtundu uliwonse wa anthu,
kuti akakhale pa dziko lonse lapansi; ndipo Iye anakonzeratu nthawi yawo
ndiponso malo enieni kumene adzakhale. 27 Mulungu anachita izi kuti
anthu amufunefune, ndikuti pomufunafunapo amupeze ngakhale kuti Iye

sali kutali ndi aliyense wa ife. 28 ‘Pakuti timakhala mwa Iye, kuyenda mwa
Iye ndi kukhala moyo mwa Iye.’ Monga olemba ndakatulo anu ena akuti,
‘Ife ndi zidzukulu zake.’
29 “Tsono popeza ndife ana a Mulungu, tisaganize kuti umulungu
wake ndi wofanana ndi ndalama zagolide, zasiliva, mwala, kapenanso
fanizo lopangidwa mwaluso la nzeru za anthu. 30 Nthawi imene
anthu sankadziwa, Mulungu anawalekerera koma tsopano akulamulira
kuti anthu onse, kulikonse atembenuke mtima. 31 Pakuti Iye wayika
tsiku limene adzaweruze dziko lapansi mwa chilungamo kudzera mwa
Munthu amene anamusankha. Iye watsimikizira anthu onse zimenezi
pomuukitsa.”
32 Atamva za kuuka kwa akufa, ena a iwo anaseka, koma enanso
anati, “Ife tikufuna tidzamvenso zimenezi tsiku lina.” 33 Ndipo Paulo
anatuluka m’Bwalolo. 34 Anthu ena ochepa anamutsatira Paulo ndipo
anakhulupirira. Pakati pawo panali Dionisiyo mmodzi wa bwalo la
Areopagi ndi mayi wina wotchedwa Damalisi ndi enanso.

# 18

*Ku Korinto*

1 Zitatha izi, Paulo anachoka ku Atene ndipo anapita ku Korinto.
2 Kumeneko anakumana ndi Myuda wina dzina lake Akula, nzika ya ku
Ponto amene anali atangofika kumene kuchokera ku Italiya pamodzi ndi
mkazi wake Prisila, chifukwa Klaudiyo analamula Ayuda onse kuti achoke
ku Roma. Paulo anapita kukawaona. 3 Popeza Paulo anali m’misiri wosoka
matenti monga iwo, iye anakhala nawo namagwirira ntchito pamodzi.
4 Tsiku la Sabata lililonse Paulo amakambirana ndi anthu m’sunagoge,
kufuna kukopa Ayuda ndi Agriki.
5 Sila ndi Timoteyo atafika kuchokera ku Makedoniya, Paulo ankan-
gogwira ntchito yolalikira yokha basi, kuchitira umboni Ayuda kuti Yesu
ndiye Khristu. 6 Koma pamene Ayuda anatsutsana naye ndi kumuchita
chipongwe, iye anakutumula zovala zake nati, “Magazi anu akhale pamitu
yanu! Ine ndilibe mlandu. Kuyambira tsopano ndipita kwa anthu a
mitundu ina.”
7 Ndipo Paulo anatuluka m’sunagoge napita ku nyumba yoyandikana
ndi sunagoge ya Tito Yusto, munthu wopembedza Mulungu. 8 Krispo,
mkulu wa sunagoge, pamodzi ndi a pa banja lake lonse anakhulupirira
Ambuye; ndiponso Akorinto ambiri amene anamva Paulo akulalikira
anakhulupiriranso nabatizidwa.
9 Usiku wina Ambuye anaonekera kwa Paulo m’masomphenya na-
muwuza kuti, “Usaope, pitiriza kuyankhula, usakhale chete. 10 Pakuti Ine
ndili nawe, palibe aliyense amene adzakukhudza ndi kukuchitira choyipa,
chifukwa mu mzinda muno ndili ndi anthu ambiri.” 11 Choncho Paulo
anakhala kumeneko chaka ndi miyezi isanu ndi umodzi akuphunzitsa
Mawu a Mulungu.
12 Galiyo ali mkulu wa boma wa ku Akaya, Ayuda mogwirizana ana-
mugwira Paulo napita naye ku bwalo la milandu. 13 Iwo anati, “Munthu
uyu akukopa anthu kuti azipembedza Mulungu mwanjira zotsutsana ndi
malamulo athu.”
14 Pamene Paulo ankati ayankhule, Galiyo anati kwa Ayuda,
“Ukanakhala mlandu wochita choyipa kapena wolakwira mnzake, bwenzi
nditakumverani bwinobwino. 15 Koma popeza ndi nkhani yokhudza

mawu, mayina ndi malamulo anu, kambiranani nokhanokha. Ine
sindidzaweruza zinthu zimenezi." [16] Kotero iye anawapirikitsa m'bwalo
la milandu. [17] Kenaka iwo anagwira Sositene, mkulu wa sunagoge, ndipo
anamumenya m'bwalo la milandu momwemo. Koma Galiyo sanasamale
zimenezi.

### *Prisila, Akula ndi Apolo*

[18] Paulo anakhalabe ku Korinto masiku ambiri. Kenaka anawasiya
abale nakwera sitima ya pamadzi kupita ku Siriya, pamodzi ndi Prisila
ndi Akula. Asanakakwere sitima ya pamadzi, anameta tsitsi lake ku
Kenkreya chifukwa anali atalumbira. [19] Iwo anafika ku Efeso, kumene
Paulo anasiyako Prisila ndi Akula. Iye yekha analowa m'sunagoge
nakambirana ndi Ayuda. [20] Iwo atapempha kuti akakhale nawo nthawi
yayitali, iye anakana. [21] Koma pamene amachoka anawalonjeza kuti,
"Ndidzabweranso Mulungu akalola." Ndipo anakwera sitima ya pamadzi
kuchoka ku Efeso. [22] Pamene Paulo anafika ku Kaisareya, anakwera
kukapereka moni ku mpingo kenaka anatsikira ku Antiokeya.
[23] Atakhala kwa kanthawi ku Antiokeya, Paulo anachokako nayendera
madera onse a ku Galatiya ndi ku Frugiya kulimbikitsa ophunzira onse.

### *Za Apolo*

[24] Pa nthawi yomweyi Myuda wina dzina lake Apolo, mbadwa ya ku
Alekisandriya anafika ku Efeso. Anali munthu wophunzira ndi wodziwa
bwino Malemba. [25] Apoloyu anaphunzitsidwa njira ya Ambuye, ndipo
anayankhula ndi changu chachikulu naphunzitsa za Yesu molondola,
ngakhale amadziwa ubatizo wa Yohane wokha. [26] Iye anayamba
kuyankhula m'sunagoge molimba mtima. Pamene Prisila ndi Akula
anamva, iwo anamuyitanira ku nyumba yawo ndipo anamufotokozera
njira ya Mulungu molongosoka bwino.
[27] Pamene Apolo anafuna kupita ku Akaya, abale anamulimbikitsa,
nalemba kalata kwa ophunzira a kumeneko kuti amulandire. Atafika
kumeneko, anathandiza kwambiri amene anakhulupirira mwachisomo.
[28] Pakuti iye anatsutsa Ayuda mwamphamvu pamaso pa anthu, natsimik-
iza kuchokera m'Malemba kuti Yesu ndiye Khristu.

## 19

### *Paulo ku Efeso*

[1] Apolo ali ku Korinto, Paulo anadutsa m'mayiko a ku mtunda ndipo
anafika ku Efeso. Kumeneko anapeza ophunzira ena. [2] Iye anawafunsa
kuti, "Kodi munalandira Mzimu Woyera pamene munakhulupirira?"
Iwo anayankha kuti, "Ayi, ife sitinamvepo kuti kuli Mzimu Woyera."
[3] Tsono Paulo anawafunsa kuti, "Nanga munabatizidwa ndi ubatizo
wotani?"
Iwo anati, "Ubatizo wa Yohane."
[4] Paulo anati, "Ubatizo wa Yohane unali wa kutembenuka mtima.
Iye anawuza anthu kuti akhulupirire amene amabwera, ameneyo ndiye
Yesu." [5] Atamva zimenezi, anabatizidwa m'dzina la Ambuye Yesu.
[6] Pamene Paulo anawasanjika manja, Mzimu Woyera anadza pa iwo
ndipo anayankhula m'malilime ndipo ananenera. [7] Anthu onsewo analipo
khumi ndi awiri.
[8] Paulo analowa m'sunagoge ndipo anayankhula molimba mtima kwa
miyezi itatu, kuwatsutsa mowakopa za ufumu wa Mulungu. [9] Koma ena

anawumitsa mitima; anakana kukhulupirira ndipo ananyoza Njirayo pa
gulu la anthu. Kotero Paulo anawasiya. Iye anatenga ophunzirawo ndipo
amakambirana tsiku ndi tsiku m'sukulu ya Turano. 10 Izi zinachitika kwa
zaka ziwiri, kotero kuti Ayuda onse ndi Agriki amene amakhala ku Asiya
anamva Mawu a Ambuye.

11 Mulungu anachita zodabwitsa zapadera kudzera mwa Paulo. 12 Kotero
kuti mipango yopukutira thukuta ndi yovala pogwira ntchito, zomwe zi-
nakhudza thupi la Paulo amapita nazo kwa odwala ndipo amachiritsidwa
ndiponso mizimu yoyipa mwa iwo imatuluka.

### *Za Ana a Skeva*

13 Ayuda ena amene ankayendayenda kutulutsa mizimu yoyipa anayesa
kugwiritsa ntchito dzina la Ambuye Yesu pa amene anali ndi ziwanda. Iwo
popemphera amati, "Ine ndikulamulira utuluke, m'dzina la Yesu amene
Paulo amamulalikira." 14 Amene ankachita zimenezi anali ana asanu ndi
awiri a Skeva, mkulu wa ansembe wa Chiyuda. 15 Tsiku lina mzimu woyipa
unawayankha kuti, "Yesu ndimamudziwa ndiponso Paulo ndimamudziwa,
nanga inu ndinu ndani?" 16 Pamenepo munthu amene anali ndi mzimu
woyipa anawalumphira nawagwira onse. Iye anawamenya kwambiri,
kotero kuti anathawa m'nyumbamo ali maliseche, akututuluka magazi.

17 Ayuda ndi Agriki okhala ku Efeso atamva zimenezi, anachita
mantha, ndipo anthu anachitira ulemu dzina la Ambuye Yesu koposa.
18 Ambiri a iwo amene tsopano anakhulupirira anafika ndi kuvomereza
poyera ntchito zawo zoyipa. 19 Ambiri amene amachita za matsenga
anasonkhanitsa mabuku awo pamodzi nawatentha pamaso pa anthu
onse. Atawonkhetsa mtengo wa mabukuwo, unakwanira ndalama zasiliva
50,000. 20 Kotero Mawu a Ambuye anapitirira kufalikira ndipo anagwira
ntchito mwamphamvu.

21 Zonsezi zitachitika Paulo anatsimikiza zopita ku Yerusalemu kudzera
ku Makedoniya ndi ku Akaya. Iye anati, "Kuchokera kumeneko, ndiyenera
kukafikanso ku Roma." 22 Iye anatuma anthu awiri amene ama-
muthandiza, Timoteyo ndi Erasto ku Makedoniya, pamene iye anakhalabe
ku Asiya kwa kanthawi.

### *Chipolowe ku Efeso*

23 Pa nthawi yomweyo panachitika chipolowe chachikulu chifukwa cha
Njira ya Ambuye. 24 Mmisiri wantchito zasiliva, dzina lake Demetriyo,
amene amapanga mafano asiliva a Atemi ankabweretsa phindu lalikulu
kwa amisiri a kumeneko. 25 Iye anasonkhanitsa pamodzi amisiriwo,
pamodzinso ndi anthu ena ogwira ntchito yomweyo ndipo anati, "Anthu
inu, mukudziwa kuti ife timapeza chuma chathu kuchokera pa ntchito
imeneyi. 26 Ndipo inu mukuona ndi kumva kuti munthu uyu Paulo wakopa
ndi kusokoneza anthu ambiri a ku Efeso ndiponso pafupifupi dziko lonse
la Asiya. Iye akunena kuti milungu yopangidwa ndi anthu si milungu
ayi. 27 Choopsa ndi chakuti sikungowonongeka kwa ntchito yathu yokha
ayi, komanso kuti nyumba ya mulungu wamkulu wamkazi Atemi idzany-
ozedwa ndipo mulungu wamkazi weniweniyo amene amapembedzedwa
ku Asiya konse ndi dziko lapansi, ukulu wake udzawonongekanso."

28 Atamva zimenezi, anakwiya kwambiri ndipo anayamba kufuwula
kuti, "Wamkulu ndi Atemi." 29 Nthawi yomweyo mu mzinda wonse
munabuka chipolowe. Anthu anagwira Gayo ndi Aristariko, anzake
a Paulo a ku Makedoniya, ndipo anathamangira nawo ku bwalo la
masewero. 30 Paulo anafuna kulowa pakati pa gulu la anthu, koma

ophunzira anamuletsa. [31] Ngakhale olamulira ena aderalo, amene anali
abwenzi a Paulo, anatumiza uthenga kumuletsa kuti asayesere kulowa
m'bwalomo.
[32] Munali chisokonezo m'bwalomo pakuti ena amafuwula zina, enanso
zina. Anthu ambiri sanadziwe ngakhale chomwe anasonkhanira. [33] Ayuda
anamukankhira Alekisandro kutsogolo, ndipo ena anafuwula kumulan-
giza iye. Iye anatambasula dzanja kuti anthu akhale chete kuti afotokozere
anthu nkhaniyo. [34] Koma pamene anthuwo anazindikira kuti ndi Myuda,
onse pamodzi kwa maora awiri anafuwula kuti, "Wamkulu ndi Atemi wa
ku Efeso!"
[35] Mlembi wa mzindawo anakhazikitsa bata gulu la anthuwo ndipo
anati, "Anthu a ku Efeso, kodi ndani pa dziko lonse lapansi amene
sadziwa kuti mzinda wa Efeso umayang'anira nyumba ya mulungu
wamkulu Atemi ndi fanizo lake, limene linagwa kuchokera kumwamba?
[36] Chifukwa chake popeza zinthu izi palibe amene angazikane, inu
mukuyenera kukhala chete osachita kanthu kalikonse mofulumira. [37] Inu
mwabweretsa anthu awa pano, ngakhale kuti iwo sanabe m'nyumba
zathu zamapemphero kapena kunenera chipongwe mulungu wathu
wamkazi. [38] Ngati tsono Demetriyo ndi amisiri anzake ali ndi nkhani
ndi munthu wina aliyense, mabwalo a milandu alipo, oweruza aliponso.
Akhoza kukapereka nkhaniyo kwa oweruza milanduwo. [39] Ngati muku-
funa kubweretsa kanthu kali konse, ziyenera kukatsimikizidwa ndi bwalo
lovomerezeka. [40] Monga mmene zililimu, ife titha kuzengedwa mlandu
woyambitsa chipolowe chifukwa cha zimene zachitika lerozi. Motero ife
sitingathe kufotokoza za chipolowechi popeza palibe nkhani yake." [41] Iye
atatha kunena zimenezi anawuza gulu la anthulo kuti libalalike.

# 20

*Paulo Apita ku Makedoniya ndi ku Grisi*

[1] Litatha phokoso, Paulo anayitanitsa ophunzira ndipo atawalimbikitsa
anawatsanzika ndipo ananyamuka kupita ku Makedoniya. [2] Iye anayen-
dera madera a kumeneko, nalimbitsa mtima anthu, ndipo pomaliza pake
anapita ku Grisi. [3] Kumeneko anakhala miyezi itatu. Popeza kuti Ayuda
anakonza zomuchita chiwembu pamene amati azinyamuka kupita ku
Siriya pa sitima ya pamadzi, iye anaganiza zobwereranso kudzera ku
Makedoniya. [4] Iye anapita pamodzi ndi Sopatro mwana wa Puro wa
ku Bereya, Aristariko ndi Sekundo a ku Tesalonika, Gayo wa ku Derbe
ndi Timoteyo, ndipo a ku Asiya anali Tukiko ndi Trofimo. [5] Anthu
amenewa anatsogola ndipo anakatidikira ku Trowa. [6] Koma ife tinayenda
pa sitima ya pamadzi kuchokera ku Filipi chitatha Chikondwerero cha
Buledi wopanda Yisiti. Patapita masiku asanu tinakumana nawo enawo
ku Trowa, ndipo tinakhala kumeneko masiku asanu ndi awiri.

*Paulo Aukitsa Utiko ku Trowa*

[7] Pa tsiku loyamba la Sabata, tinasonkhana kuti tidye mgonero. Paulo
analalikira kwa anthu chifukwa anaganiza zoti achoke tsiku linalo,
ndipo analalika mpaka pakati pa usiku. [8] Munali nyale zambiri
m'chipinda chammwamba m'mene tinasonkhanamo. [9] Pa chipinda cha-
chitatu chammwamba cha nyumbayo, pa zenera, panakhala mnyamata
wina dzina lake Utiko, amene ankasinza pomwe Paulo amayankhulabe.
Atagona tulo, iye anagwa pansi kuchokera pa chipinda chammwamba

ndipo anamutola atafa. 10 Paulo anatsika, nadziponya pa mnyamatayo,
namukumbatira. Paulo anati, "Musadandaule, ali moyo!" 11 Kenaka Paulo
anakweranso, m'chipinda muja nanyema buledi nadya. Atayankhula
mpaka kucha, anachoka. 12 Anthu anatenga mnyamatayo kupita kwawo
ali moyo ndipo anatonthozedwa mtima kwambiri.

### *Paulo Alawirana ndi Akulu Ampingo a ku Efeso*

13 Ife tinatsogola kukakwera sitima ya pa madzi kupita ku Aso,
kumene tinayembekeza kukatenga Paulo. Iye anakonza motero chifukwa
amayenda wapansi. 14 Pamene anakumana nafe ku Aso tinamutenga
ndipo tinapita ku Mitilene. 15 Mmawa mwake tinachoka kumeneko
pa sitima ya pamadzi ndipo tinafika pafupi ndi Kiyo. Tsiku linalo
tinawolokera ku Samo, ndipo tsiku linanso tinafika ku Mileto. 16 Paulo
anali atatsimikiza kuti alambalale Efeso kuopa kutaya nthawi ku Asiya,
pakuti ankafulumira kuti akafike ku Yerusalemu kuti ngati n'kotheka kuti
tsiku la Pentekosite akakhale ali ku Yerusalemu.
17 Paulo ali ku Mileto, anatumiza mawu ku Efeso kuyitana akulu
ampingo. 18 Iwo atafika, Paulo anati, "Inu mukudziwa mmene nd-
inakhalira nanu nthawi yonse imene ndinali nanu kuyambira tsiku
loyamba limene ndinafika ku Asiya. 19 Ndinatumikira Ambuye modzichep-
etsa kwambiri ndiponso ndi misozi, ngakhale ndinayesedwa kwambiri ndi
ziwembu za Ayuda. 20 Inu mukudziwa kuti, sindinakubisireni kanthu ka-
likonse kopindulitsa koma ndinakuphunzitsani poyera komanso nyumba
ndi nyumba. 21 Ine ndinawuza Ayuda komanso Agriki kuti ayenera
kutembenukira kwa Mulungu polapa ndikuti akhulupirire Ambuye athu
Yesu.
22 "Ndipo tsopano, mokakamizidwa ndi Mzimu, ndikupita ku
Yerusalemu, sindikudziwa zimene zikandichitikire kumeneko."
23 Chimene ndikudziwa ndi chakuti Mzimu Woyera wandichenjeza
mu mzinda uliwonse kuti ndende ndi mavuto zikundidikira. 24 Koma
sindilabadira konse za moyo wanga ngati kuti ndi wa mtengo wapatali
kwa ine, malingana ndikatsirize ntchito yanga ndi utumiki umene
Ambuye Yesu anandipatsa, ntchito yochitira umboni Uthenga Wabwino
wachisomo cha Mulungu.
25 "Tsopano ndikudziwa kuti inu nonse amene ndinakuyenderani ndi
kumakulalikirani ufumu wa Mulungu simudzaonanso nkhope yanga.
26 Chifukwa chake, ine ndikukuwuzani lero kuti ndilibe mlandu
ndi munthu aliyense. 27 Pakuti sindinakubisireni pokulalikirani chi-
funiro chonse cha Mulungu. 28 Mudziyang'anire nokha ndiponso
muyang'anire gulu lankhosa limene Mzimu Woyera anakuyikani kuti
mukhale oyang'anira ake. Khalani abusa a mpingo wa Mulungu umene
Iye anawugula ndi magazi ake. 29 Ndikudziwa kuti ndikachoka ine,
padzafika mimbulu yolusa pakati panu imene sidzalekerera gulu lankhos-
alo. 30 Ngakhale pakati pa inu nokha padzapezeka anthu oyankhula
zonama ndi cholinga chofuna kukhala ndi ophunzira kuti awatsate.
31 Tsono inu, samalani! Kumbukirani kuti kwa zaka zitatu, usana ndi usiku
ndiponso ndi misozi sindinaleke kuchenjeza aliyense wa inu.
32 "Tsopano ine ndikukuperekani kwa Mulungu ndiponso kwa mawu
a chisomo chake, amene ali ndi mphamvu zokulitsa inu ndi kukupatsani
chuma pakati pa onse amene anayeretsedwa. 33 Ine sindinasirire siliva
kapena golide kapena zovala za munthu aliyense. 34 Inu nomwe

mukudziwa kuti manja angawa ananditumikira kuti tipeze zimene ine
ndi anzanga tinkazifuna. 35 Pa zonse zimene ndinachita, ndinakuonetsani
kuti pogwira ntchito molimbika motere tiyenera kuthandiza ofowoka,
pokumbukira mawu a Ambuye Yesu akuti, 'Kupereka kumadalitsa kuposa
kulandira.' "
36 Atanena zimenezi, anagwada pansi pamodzi ndi ena onse, napem-
phera. 37 Onse analira pamene amamukumbatira ndi kupsompsona.
38 Chimene chinamvetsa chisoni kwambiri ndi mawu ake akuti sadzao-
nanso nkhope yake. Kenaka iwo anamuperekeza ku sitima yapamadzi.

# 21

*Paulo Apita ku Yerusalemu*

1 Titalawirana nawo, tinachoka kumeneko m'sitima ya pamadzi, ndipo
tinayenda molunjika mpaka kufika ku Kosi. Mmawa mwake tinapita ku
Rode, kuchokera kumeneko tinapita ku Patara. 2 Kumeneko tinapeza
sitima yapamadzi yopita ku Foinike. Choncho tinalowamo n'kunyamuka.
3 Tinaona chilumba cha Kupro ndipo tinadutsa kummwera kwake n'kupita
ku Siriya. Tinakayima ku Turo chifukwa sitima yathuyo imayenera
kusiya katundu kumeneko. 4 Tinafunafuna ophunzira kumeneko, ndipo
titawapeza tinakhala nawo masiku asanu ndi awiri. Iwowa, mwa Mzimu
Woyera anakakamiza Paulo kuti asapite ku Yerusalemu. 5 Koma nthawi
yathu itatha, tinachokako ndi kupitiriza ulendo wathu. Ophunzira onse
pamodzi ndi akazi awo ndi ana anatiperekeza mpaka kunja kwa mzinda.
Ndipo kumeneko tinagwada m'mbali mwa nyanja ndi kupemphera.
6 Titatsanzikana, tinalowa m'sitima ija, iwowo anabwerera ku nyumba
zawo.
7 Ife tinapitiriza ulendo wathu wochokera ku Turo mpaka tinafika ku
Ptolemayi. Kumeneko tinalonjera abale ndi kukhala nawo tsiku limodzi.
8 Tinachoka mmawa mwake, mpaka tinakafika ku Kaisareya. Tinapita
kukakhala m'nyumba ya mlaliki Filipo, amene anali mmodzi mwa atumiki
a mpingo asanu ndi awiri aja. 9 Iye anali ndi ana aakazi anayi osakwatiwa
amene anali ndi mphatso ya uneneri.
10 Titakhala kumeneko masiku ambiri, kunabwera mneneri wina
wochokera ku Yudeya dzina lake Agabu. 11 Atafika kwa ife, anatenga
lamba wa Paulo, nadzimanga naye manja ake ndi mapazi ake ndipo anati,
"Mzimu Woyera akuti, 'Mwini lambayu, Ayuda adzamumanga chomwechi
ku Yerusalemu, ndipo adzamupereka m'manja mwa anthu a mitundu
ina.' "
12 Titamva zimenezi, ife pamodzi ndi anthu kumeneko tinamudan-
daulira Paulo kuti asapite ku Yerusalemu. 13 Koma Paulo anayankha kuti,
"Chifukwa chiyani mukulira ndi kunditayitsa mtima? Ndine wokonzeka
osati kumangidwa kokha ayi, komanso kufa ku Yerusalemu chifukwa cha
dzina la Ambuye Yesu." 14 Titalephera kumuletsa tinamuleka ndipo tinati,
"Chifuniro cha Ambuye chichitike."
15 Pambuyo pake, ife tinakonzeka ndi kunyamuka kumapita ku
Yerusalemu. 16 Ena mwa ophunzira a ku Kaisareya anatiperekeza mpaka
kukatifikitsa ku nyumba ya Mnasoni, kumene tinakonza kuti tizikhalako.
Iye anali wa ku Kupro ndiponso mmodzi wa ophunzira oyambirira.

*Paulo Afika ku Yerusalemu*

17 Titafika ku Yerusalemu, abale anatilandira mwachimwemwe.
18 Mmawa mwake Paulo pamodzi ndi ife tonse tinapita kwa Yakobo,
ndipo akulu onse a mpingo anali komweko. 19 Paulo anawalonjera ndi
kuwafotokozera mwatsatanetsatane zimene Mulungu anachita pakati pa
anthu a mitundu ina kudzera mu utumiki wake.
20 Atamva zimenezi, iwo anayamika Mulungu. Kenaka anawuza Paulo
kuti, “M’bale, ukuona kuti pali Ayuda ambirimbiri amene anakhulupirira,
ndipo ndi okhulupirika potsatira Malamulo a Mose. 21 Iwo anawuzidwa
kuti iwe umaphunzitsa Ayuda onse amene akukhala pakati pa anthu a
mitundu ina kuti asiye kutsatira Mose, kuti asamachite mdulidwe kapena
kutsatira miyambo. 22 Nanga pamenepa ife titani? Iwo adzamva ndithu
kuti iwe wabwera, 23 tsono iwe chita zimene ife tikuwuze. Tili nawo
amuna anayi pano amene anachita lumbiro kwa Mulungu. 24 Muwatenge
anthu amenewa, ndipo muchite nawo mwambo wowayeretsa ndipo
muwalipirire zoti apereke kuti amete tsitsi lawo. Kotero aliyense
adzadziwa kuti palibe choonadi pa zimene anamva za inu, koma kuti inu
mwini mumakhala moyo womvera Malamulo. 25 Koma kunena za anthu
a mitundu ina amene asandulika okhulupirira, ife tinawalembera zimene
tinavomerezana zakuti asadye chakudya choperekedwa ku mafano,
asadye magazi, asadye nyama yopotola ndiponso asachite zadama.”
26 Mmawa mwake Paulo anatenga amuna aja ndipo anachita mwambo
wodziyeretsa. Kenaka anapita ku Nyumba ya Mulungu nakadziwitsa
ansembe za tsiku limene adzatsiriza nthawi ya kudziyeretsa ndi kuperekera nsembe aliyense wa iwo.

### *Agwira Paulo*

27 Ali pafupi kutsiriza masiku asanu ndi awiriwo, Ayuda ena ochokera
ku Asiya anaona Paulo m’Nyumba ya Mulungu. Iwo anawutsa gulu
lonse la anthu ndipo anamugwira Paulo, 28 akufuwula kuti, “Inu Aisraeli,
tithandizeni! Ndi uyu munthu uja amaphunzitsa anthu onse ponseponse
kuti azinyoza mtundu wathu ndiponso Malamulo athu ndi malo ano.
Kuwonjezera pamenepo, walowetsa Agriki m’bwalo la Nyumba ino ndipo
wadetsa malo opatulika.” 29 Iwo ananena izi chifukwa anali ataona
Trofimo wa ku Efeso ali ndi Paulo mu mzindamo ndipo iwo ankaganiza
kuti Paulo anamulowetsa m’bwalo la Nyumba ya Mulungu.
30 Mzinda wonse unasokonezeka, ndipo anthu anabwera akuthamanga
kuchokera kumbali zonse. Anamugwira Paulo, namukokera kunja kwa
Nyumbayo, ndipo nthawi yomweyo anatseka zipata. 31 Pamene anthuwo
ankafuna kupha Paulo, nkhaniyi inamveka kwa mkulu wa magulu a
asilikali a Aroma kuti mzinda wonse wa Yerusalemu wasokonezeka.
32 Nthawi yomweyo iye anatenga asilikali ndi atsogoleri a magulu a
asilikali ndi kuthamangira kumene kunali anthuwo. Anthuwo ataona
mkuluyo ndi asilikali ake analeka kumenya Paulo.
33 Mkulu wa asilikaliyo anabwera nagwira Paulo, ndipo analamula
kuti amangidwe ndi maunyolo awiri. Kenaka iye anafunsa kuti ndi
ndani ndipo wachita chiyani. 34 Ena m’gulumo anafuwula chinthu
china ndi enanso chinanso. Tsono popeza mkulu wa asilikaliyo sanathe
kudziwa choonadi chenicheni chifukwa cha phokoso, analamula kuti
Paulo atengedwe kupita ku malo a asilikali. 35 Paulo atafika pa makwerero
olowera ku malo a asilikaliwo, ananyamulidwa ndi asilikali chifukwa cha
ukali wa anthuwo. 36 Gulu la anthu limene linamutsatira linapitiriza
kufuwula kuti, “Ameneyo aphedwe basi!”

### *Paulo Ayankhula*

37 Asilikali ali pafupi kulowa naye ku malo awo, iye anapempha mkulu
wa asilikaliyo kuti, “Kodi mungandilole ndiyankhulepo?”
Mkulu wa asilikaliyo anafunsa kuti, “Kodi umayankhula Chigriki?
38 Kodi sindiwe Mwigupto uja amene masiku apitawo unayambitsa
kuwukira ndi kutsogolera anthu 4,000 owukira aja n’kupita nawo ku
chipululu?”
39 Paulo anayankha kuti, “Ine ndine Myuda, wa ku Tarisisi ku Kilikiya.
Sindine nzika ya mzinda wamba. Chonde loleni ndiyankhule nawo
anthuwa.”
40 Ataloledwa ndi mkulu wa asilikaliyo, Paulo anayimirira pa makw-
ereropo nakweza dzanja lake kwa gulu la anthuwo. Onse atakhala chete,
iye anayankhula nawo m’Chihebri.

## 22

1 Iye anati, “Inu abale anga ndi makolo anga, tamvani mawu
akudziteteza kwanga.” 2 Atamva iye akuyankhula Chihebri, anakhala
chete.
Kenaka Paulo anati, 3 “Ine ndine Myuda, wobadwira ku Tarisisi wa
ku Kilikiya, koma ndinaleredwa mu mzinda muno, ndinaphunzitsidwa
mwatsatanetsatane kusunga malamulo a makolo athu ndi Gamalieli ndipo
ndinali wodzipereka pa za Mulungu monga mmene inu mulili lero. 4 Ine
ndinkazunza anthu otsatira Njirayi mpaka kuwapha. Ndinkagwira amuna
ndi amayi ndi kuwayika m’ndende. 5 Mkulu wa ansembe ndiponso
akuluakulu a Ayuda angathe kundichitira umboni. Iwowa anandipatsa
makalata opita nawo kwa abale awo ku Damasiko. Ndipo ndinapita
kumeneko kuti ndikawagwire anthu amenewa ndi kubwera nawo ku
Yerusalemu kuti adzalangidwe.
6 “Nthawi ya masana, nditayandikira ku Damasiko, mwadzidzidzi
kuwala kwakukulu kochokera kumwamba kunandizungulira. 7 Ndinagwa
pansi ndipo ndinamva mawu akuti, ‘Saulo! Saulo! Ukundizunziranji?’ ”
8 Ine ndinafunsa kuti, “Ndinu ndani Ambuye?”
Iye anayankha kuti, “Ndine Yesu wa ku Nazareti, amene iwe uku-
muzunza.” 9 Anzanga a paulendo anaona kuwalako, koma sanamve
mawuwo, a Iye amene amayankhula nane.
10 Ine ndinafunsa kuti, “Kodi ndichite chiyani Ambuye?”
Ambuye anati, “Imirira ndipo pita ku Damasiko. Kumeneko adza-
kuwuza zonse zimene ukuyenera kuchita.” 11 Anzanga anandigwira
dzanja kupita nane ku Damasiko, popeza kuwala kunja kunandichititsa
khungu.
12 “Munthu wina dzina lake Hananiya anabwera kudzandiona. Iyeyu
anali munthu woopa Mulungu ndi wosunga Malamulo. Ayuda onse
okhala kumeneko amamupatsa ulemu waukulu. 13 Iye anayimirira pafupi
nane nati, ‘M’bale Saulo, penyanso!’ Ndipo nthawi yomweyo ndinapenya
ndikumuona iyeyo.
14 “Ndipo iye anati, ‘Mulungu wa makolo athu wakusankha iwe kuti
udziwe chifuniro chake ndi kuona Wolungamayo ndi kumva mawu
ochokera pakamwa pake. 15 Iwe udzakhala mboni yake kwa anthu onse
pa zimene waziona ndi kuzimva. 16 Ndipo tsopano ukudikira chiyani?
Dzuka ndi kutama dzina la Ambuye mopemba, ubatizidwe ndi kuchotsa
machimo ako.’

17 “Nditabwerera ku Yerusalemu, ndikupemphera m’Nyumba ya Mu-
lungu, ndinachita ngati ndakomoka. 18 Ndinaona Ambuye akundiwuza
kuti, ‘Fulumira! Tuluka mu Yerusalemu msangamsanga, chifukwa
anthuwa sadzavomereza umboni wako wonena za Ine.’ ”
19 Ine ndinayankha Ambuye kuti, “Anthu awa akudziwa kuti ine
ndinkapita ku sunagoge iliyonse ndipo ndinkawaponya m’ndende ndi
kuwakwapula amene ankakhulupirira inu. 20 Ndipo pamene ankapha
Stefano, ine ndinali pomwepo kuvomereza ndi kusunga zovala za amene
amamupha.”
21 Pamenepo Ambuye anandiwuza kuti, “Nyamuka; Ine ndidzakutuma
kutali kwa anthu a mitundu ina.”

### *Paulo Nzika ya Chiroma*

22 Gulu la anthu linamvetsera mawu a Paulo mpaka pamene ananena
izi, kenaka anakweza mawu awo nafuwula kuti, “Ameneyo aphedwe basi!
Ngosayenera kukhala moyo!”
23 Akufuwula ndi kuponya zovala zawo ndi kuwaza fumbi kumwamba,
24 mkulu wa asilikali analamulira kuti amutenge Paulo kupita naye ku
malo a asilikali. Iye analamula kuti Paulo akwapulidwe kwambiri ndi ku-
mufunsa kuti apeze chimene anthu ankafuwulira chotere. 25 Atamumanga
kuti amukwapule, Paulo anati kwa msilikali wolamulira asilikali 100
amene anayima pamenepo, “Kodi malamulo amalola kukwapula nzika ya
Chiroma imene sinapezedwe yolakwa?”
26 Wolamulira asilikali 100 uja atamva zimenezi, anapita kwa mkulu wa
asilikali ndi kumufotokozera. Iye anafunsa kuti, “Kodi mukuchita chiyani
ndi munthuyu amene ndi nzika ya Chiroma?”
27 Mkulu wa asilikali uja anapita kwa Paulo ndipo anamufunsa kuti,
“Tandiwuze, kodi ndiwe nzika ya Chiroma?”
Paulo anayankha kuti, “Inde.”
28 Kenaka mkulu wa asilikaliyo anati, “Ine ndinapereka ndalama
zambiri kuti ndikhale nzika.”
Paulo anayankha kuti, “Koma ine ndinabadwa nzika.”
29 Iwo amene anati amufunse analeka nthawi yomweyo. Mkulu wa
asilikali uja anachita mantha atazindikira kuti wamanga Paulo amene ndi
nzika ya Chiroma.

### *Paulo ku Bwalo Lalikulu la Ayuda*

30 Mmawa mwake, mkulu wa asilikali pofuna kupeza chifukwa
chenicheni chimene Ayuda amamunenera Paulo, anamumasula ndipo
analamula kuti akulu a ansembe ndi onse akuluakulu a Bwalo Lalikulu
asonkhane. Ndipo iye anabweretsa Paulo namuyimiritsa patsogolo pawo.

## 23

1 Paulo anayang’anitsitsa anthu a Bwalo Lalikulu nati, “Abale anga,
ndakhala ndi chikumbumtima chabwino pamaso pa Mulungu mpaka lero
lino.” 2 Chifukwa cha mawu amenewa, mkulu wa ansembe Ananiya
analamulira amene anali pafupi ndi Paulo kuti amumenye pakamwa.
3 Pamenepo Paulo anamuwuza kuti, “Mulungu adzakukantha, iwe munthu
wachiphamaso! Wakhala pamenepo kuti undiweruze ine monga mwala-
mulo, koma iweyo ukuphwanya lamulolo polamulira kuti andimenye!”
4 Anthu amene anayimirira pafupi ndi Paulo anati, “Bwanji ukunyoza
mkulu wa ansembe wa Mulungu?”

5 Paulo anayankha nati, “Abale, ine sindinazindikire kuti ndi mkulu
wa ansembe; pakuti kunalembedwa kuti, ‘Usayankhule zoyipa kwa
mtsogoleri wa anthu ako.’ ”

6 Paulo atazindikira kuti ena mwa iwo anali Asaduki ndiponso ena anali
Afarisi, anafuwula m’bwalo muja kuti, “Abale anga, ine ndine Mfarisi,
mwana wa Mfarisi. Ndikuweruzidwa chifukwa cha chiyembekezo cha
kuuka kwa akufa.” 7 Iye atanena zimenezi, mkangano unabuka pakati
pa Afarisi ndi Asaduki mpaka anthu kugawikana. 8 Asaduki amati kulibe
kuuka kwa akufa, kulibenso ngakhale angelo kapena mizimu, koma
Afarisi amakhulupirira zonsezi.

9 Panali phokoso lalikulu, ndipo aphunzitsi ena amalamulo amene anali
a gulu la Afarisi anayimirira natsutsa kwambiri. Iwo anati, “Ife sitikupeza
cholakwa ndi munthu uyu, chifukwa mwina ndi mzimu kapena mngelo
amene wayankhula naye.” 10 Mkangano unakula kwambiri kotero kuti
mkulu wa asilikali anachita mantha kuti mwina anthu angakhadzule
Paulo. Iye analamulira asilikali ake apite kukamuchotsa pakati pawo
mwamphamvu ndi kubwera naye ku malo a asilikaliwo.

11 Usiku omwewo Ambuye anayimirira pambali pa Paulo nati, “Limba
mtima! Monga wandichitira Ine umboni mu Yerusalemu, moteronso
uyenera kundichitira umboni ku Roma.”

### *Ayuda Achita Chiwembu Paulo*

12 Kutacha Ayuda ena anakonza chiwembu ndipo analumbira kuti
sadya kapena kumwa mpaka atapha Paulo. 13 Anthu amene anakonza
chiwembuchi analipo makumi anayi. 14 Iwo anapita kwa akulu a ansembe
ndi akuluakulu a Ayuda nakawawuza kuti, “Ife talumbira kolimba
kuti sitidya kalikonse mpaka titapha Paulo. 15 Tsopano inu pamodzi
ndi akuluakulu a Bwalo Lalikulu mupemphe mkulu wa asilikali kuti
akubweretsereni Paulo ngati kuti mukufuna kudziwa bwino za mlandu
wake. Ife takonzeka kudzamupha asanafike kumeneko.”

16 Koma mwana wa mlongo wake wa Paulo atamva za chiwembuchi,
anapita ku malo a asilikali aja namufotokozera Paulo.

17 Paulo anayitana mmodzi wa wolamulira asilikali 100 aja, namuwuza
kuti, “Pita naye mnyamatayu kwa mkulu wa asilikali. Iyeyu ali ndi mawu
oti akamuwuze.” 18 Anamutengadi mnyamatayo napita naye kwa mkulu
wa asilikali uja, nati, “Wam’ndende uja Paulo anandiyitana, nandipempha
kuti ndibweretse mnyamatayu kwa inu chifukwa ali ndi kanthu koti
akuwuzeni.”

19 Mkulu wa asilikali uja anagwira dzanja mnyamatayo napita naye
paseli ndipo anamufunsa kuti, “Kodi ukufuna kuti undiwuze chiyani?”

20 Mnyamatayo anati, “Ayuda agwirizana zoti akupempheni kuti mawa
mubwere ndi Paulo ku Bwalo Lalikulu, ngati kuti akufuna kudziwa bwino
za iye. 21 Inu musawamvere, chifukwa pali anthu opitirira makumi
anayi amene akumudikirira pa njira. Iwo alumbira kuti sadya kapena
kumwa mpaka atapha Paulo. Panopa ndi okonzeka kale, akungodikira
kuti muwavomere pempho lawo.”

22 Mkulu wa asilikaliyo anawuza mnyamatayo kuti apite koma ana-
muchenjeza kuti, “Usawuze munthu aliyense kuti wandifotokozera
zimenezi.”

### *Paulo Apita ku Kaisareya*

23 Kenaka mkulu wa asilikaliyo anayitana awiri a asilikali olamulira
asilikali 100 nawalamula kuti, “Uzani asilikali 200, asilikali 70 okwera pa
akavalo ndi 200 onyamula mikondo kuti akonzeke kupita ku Kaisareya
usiku omwe uno nthawi ya 9 koloko. 24 Mumukonzerenso Paulo akavalo
woti akwerepo kuti akafike bwino kwa bwanamkubwa Felike.”
25 Iye analemba kalata iyi:
26 Ine Klaudiyo Lusiya,
Kwa wolemekezeka, bwanamkubwa Felike:
Ndikupereka moni.

27 Munthuyo Ayuda anamugwira ndipo anali pafupi kumupha, koma
ine ndinapita ndi asilikali n’kukamulanditsa pakuti ndinamva kuti ndi
nzika ya Chiroma. 28 Ndinkafuna kudziwa mlandu umene anapalamula,
choncho ndinapita naye ku Bwalo lawo Lalikulu. 29 Ine ndinapeza
kuti amamuyimba mlandu wa nkhani ya malamulo awo, koma
panalibe mlandu woyenera kumuphera kapena kumuyika m’ndende.
30 Nditawuzidwa kuti amukonzera chiwembu munthuyu, ine ndamu-
tumiza kwa inu msanga. Ine ndalamulanso amene akumuyimba
mlanduwo kuti abwere kwa inu kudzafotokoza nkhaniyo.
31 Pamenepo asilikali aja anatenga Paulo monga anawalamulira napita
naye ku Antipatri usiku. 32 Mmawa mwake iwo anabwerera ku malo a
asilikali nasiya okwera pa akavalo kuti apitirire ndi Paulo. 33 Asilikali
okwera pa akavalowo atafika ku Kaisareya anapereka kalatayo kwa
bwanamkubwa, namuperekanso Paulo. 34 Bwanamkubwayo anaw-
erenga kalatayo ndipo anamufunsa Paulo za dera limene amachokera.
Atazindikira kuti amachokera ku Kilikiya, 35 iye anati, “Ndidzamva
mlandu wako okuyimba mlandu akabwera kuno.” Ndipo analamulira kuti
asilikali adzimulondera Paulo ku nyumba ya mfumu Herode.

# 24

*Felike Amva Mlandu wa Paulo*

1 Patapita masiku asanu mkulu wa ansembe Hananiya, pamodzi ndi
akuluakulu ena ndi katswiri woyankhulira anthu pa milandu wotchedwa
Tertuliyo anapita ku Kaisareya ndipo anafotokoza mlandu wa Paulo kwa
Bwanamkubwayo. 2 Atamuyitana Paulo, ndipo Tertuliyo anafotokozera
Felike nkhani yonse ya Paulo. Iye anati, “Wolemekezeka, ife takhala
pamtendere nthawi yayitali chifukwa cha inu, ndipo utsogoleri wanu
wanzeru wabweretsa kusintha m’dziko lino. 3 Wolemekezeka Felike ife
timazilandira zimenezi moyamika kwambiri ponseponse ndi mwa njira
iliyonse. 4 Koma kuti tisakuchedwetseni, ndikupempha kuti mwa kuleza
mtima kwanu mutimvere ife.
5 “Ife tapeza kuti munthu uyu amayambitsa mavuto ndi kuwutsa
mapokoso pakati pa Ayuda onse a dziko lonse lapansi. Iyeyu ndi
mtsogoleri wa mpatuko wa Anazareti. 6 Anayesera ngakhale kudetsa
Nyumba ya Mulungu wathu. Ndiye ife tinamugwira. 7 Koma, mkulu
wa asilikali Lusiya anafika mwamphamvu namuchotsa m’manja mwathu.
8 Ndipo Lusiya analamula kuti amene anali naye ndi mlandu abwere
kwa inu. Mukamufunsa ameneyu kwa nokha mudzadziwa choonadi cha
zimene ife tikumunenera.”
9 Ayuda anavomereza nanenetsa kuti zimenezi zinali zoona.

10 Bwanamkubwayo atakodola Paulo ndi kulola kuti ayankhule, Pauloyo
anati, “Ine ndikudziwa kuti inu mwakhala mukuweruza dziko lino zaka
zambiri, kotero ndikukondwera kuti ndikudziteteza ndekha pamaso panu.
11 Inu mukhoza kupeza umboni wake. Sipanapite masiku khumi ndi awiri
chipitireni changa ku Yerusalemu kukapembedza. 12 Amene akundiyimba
mlanduwa sanandipeze m’Nyumba ya Mulungu ndi kutsutsana ndi
wina aliyense kapena kuyambitsa chisokonezo m’sunagoge kapena pena
paliponse mu mzindamo. 13 Ndipo sangathe kupereka umboni wa
mlandu umene akundiyimba inewu. 14 Komatu ine ndikuvomera kuti
ndimapembedza Mulungu wa makolo athu, monga wotsatira wa Njirayo,
imene iwo akuyitchula mpatuko. Ine ndimakhulupirira chilichonse
chimene chimagwirizana ndi malamulo ndiponso zimene zinalembedwa
ndi Aneneri. 15 Ine ndili nacho chiyembekezo chomwecho chimene iwo ali
nacho mwa Mulungu, kuti kudzakhala kuuka kwa akufa kwa olungama
ndiponso kwa ochimwa. 16 Kotero ine ndimayesetsa kuti ndikhale ndi
chikumbumtima chosanditsutsa pamaso pa Mulungu ndi anthu onse.

17 “Patapita zaka zambiri, ndinabwera ku Yerusalemu kudzapereka
mphatso kwa anthu osauka a mtundu wanga komanso kudzapereka
nsembe. 18 Pamene ndinkachita zimenezi, iwo anandipeza m’bwalo la
Nyumba ya Mulungu nditachita mwambo wodziyeretsa. Panalibe gulu
la anthu kapena kuti ndimachita za chisokonezo chilichonse. 19 Koma
pali Ayuda ena ochokera ku Asiya, amene amayenera kukhala pano
pamaso panu, kundiyimba mlandu ngati ali ndi kalikonse konditsutsa ine.
20 Kapena awa amene ali panowa anene mlandu umene anapeza mwa ine,
pamene ndinayima pamaso pa Bwalo lawo Lalikulu. 21 Koma cholakwa
changa chingathe kukhala chokhachi chakuti, nditayima pamaso pawo
ndinafuwula kuti, ‘Mukundiweruza ine lero chifukwa ndimakhulupirira
kuti akufa adzauka.’ ”

22 Kenaka Felike, amene amadziwa bwino za Njirayo, anayamba wayim-
itsa mlanduwo, nati, “Ndidzagamula mlandu wako akabwera mkulu
wa asilikali Lusiya.” 23 Iye analamulira woyang’anira asilikali 100 kuti
alondere Paulo, koma azimupatsako ufulu ndiponso kulola abwenzi ake
kuti adzimusamalira.

24 Patapita masiku angapo Felike anabwera pamodzi ndi mkazi wake
Drusila, amene anali Myuda. Anayitana Paulo ndipo anamvetsera zimene
amayankhula za chikhulupiriro mwa Khristu Yesu. 25 Paulo atayankhula
za chilungamo, za kudziretsa ndiponso za chiweruzo chimene chikub-
wera, Felike anachita mantha ndipo anati, “Basi tsopano! Pita. Tidza-
kuyitanitsa tikadzapeza mpata.” 26 Pa nthawi imeneyi amayembekeza
kuti Paulo adzamupatsa ndalama, n’chifukwa chake amamuyitanitsa
kawirikawiri ndi kumayankhula naye.

27 Patapita zaka ziwiri, Porkiyo Festo analowa m’malo mwa Felike, koma
anamusiya Paulo m’ndende, chifukwa amafuna kuti Ayuda amukonde.

## 25

*Paulo ku Bwalo la Milandu la Festo*

1 Patapita masiku atatu Festo atafika m’dera lake, anachoka ku Kaisareya
ndi kupita ku Yerusalemu. 2 Kumeneko akulu a ansembe ndi atsogoleri
a Chiyuda anabwera kwa iye ndi kumufotokozera mlandu wa Paulo.
3 Iwo anamupempha Festo kuti awakomere mtima potumiza Paulo ku
Yerusalemu, pakuti anali atakonzekera chiwembu kuti amuphe Pauloyo

pa njira. [4] Festo anayankha kuti, "Paulo akusungidwa ku Kaisareya, ndipo
ndipita kumeneko posachedwa. [5] Ena mwa atsogoleri anu apite nane
kumeneko, kuti akafotokoze mlandu wa munthuyu, ngati anachita kanthu
kalikonse kolakwika."

[6] Festo atakhala nawo masiku asanu ndi atatu kapena khumi iye anapita
ku Kaisareya, ndipo mmawa mwake anayitanitsa bwalo nalamula kuti
abweretse Paulo pamaso pake. [7] Paulo atafika, Ayuda amene anafika
kuchokera ku Yerusalemu anayima momuzungulira. Iwo anamunenera
zinthu zoopsa zambiri zimene sakanatha kubweretsa umboni wake.

[8] Kenaka Paulo ananena mawu ake odziteteza kuti, "Ine sindinalak-
wirepo lamulo la Ayuda, kapena Nyumba ya Mulungu kapenanso Kaisara."

[9] Festo, pofuna kuti Ayuda amukonde anafunsa Paulo kuti, "Kodi iwe
ukufuna kupita ku Yerusalemu, kuti kumeneko ukafotokoze mlandu wako
pamaso panga?"

[10] Paulo anayankha kuti, "Ine tsopano ndayima pamaso pa bwalo la mi-
landu la Kaisara, ndiko kumene ayenera kundiweruza. Ine sindinalakwire
Ayuda, monga inu mukudziwa bwino. [11] Koma ngati ndili wolakwa, ngati
ndachita kanthu koyenera kuphedwa, ine sindikukana kufa. Koma ngati
mlandu umene abweretsa Ayudawa siwoona, palibe munthu angathe
kundipereka m'manja mwawo. Ndikupempha kuti ndikaweruzidwe ndi
Kaisara!"

[12] Festo atakambirana ndi akuluakulu abwalo lake, anati, "Popeza
wapempha kupita kwa Kaisara, kwa Kaisara udzapitadi!"

### *Festo Afotokozera Mfumu Agripa*

[13] Patapita masiku ochepa mfumu Agripa pamodzi ndi Bernisi anabwera
ku Kaisareya kudzalonjera Festo. [14] Atakhala kumeneko masiku angapo,
Festo anafotokozera mfumuyo za mlandu wa Paulo. Iye anati, "Kuli
munthu wina kuno amene Felike anamusiya m'ndende. [15] Nditapita ku
Yerusalemu akulu a ansembe ndi akuluakulu a Ayuda anandifotokozera
mlandu wake ndipo anandipempha kuti ndigamule kuti ndi wolakwa.

[16] "Ine ndinawayankha kuti si mwambo wa Aroma kungomupereka
munthu ayi. Munthu woyimbidwa mlanduyo amayenera kukumana
nawo omunenezawo, kuti iye akhale ndi mwayi woyankhapo pa zimene
akumuyimba mlanduzo. [17] Atabwera kuno pamodzi ndi ine, sindi-
nachedwetse mlanduwo, koma ndinayitanitsa bwalo mmawa mwake
ndi kulamula kuti amubweretse munthuyo. [18] Omuyimba mlandu aja
atayimirira kuti ayankhule, iwo sananene cholakwa chilichonse chimene
ndimayembekezera. [19] M'malo mwake, anatsutsana naye pa fundo zina
za chipembedzo chawo ndi za munthu wakufa, dzina lake Yesu, amene
Paulo akuti ali moyo. [20] Ine ndinathedwa nzeru wosadziwa momwe
ndikanafufuzira nkhaniyi; kotero ndinafunsa ngati akanafuna kupita ku
Yerusalemu kuti akaweruzidwe kumeneko. [21] Koma Paulo anapempha
kuti akaonekere pamaso pa mfumu ya Chiroma, ndipo ndinalamula kuti
asungidwe mpaka pamene ndidzamutumize kwa Kaisara."

[22] Ndipo Agripa anati kwa Festo, "Ine ndikufuna ndimumve ndekha
munthu ameneyu." Iye anayankha kuti, "Mudzamumva mawa."

### *Paulo Pamaso pa Agripa*

[23] Mmawa mwake Agripa ndi Bernisi anabwera mwaulemu waukulu
waufumu nalowa m'bwalo la milandu pamodzi ndi akulu a asilikali
ndiponso akuluakulu a mu mzindawo. Atalamula Festo kuti Paulo

abwere, anabweradi. 24 Festo anati, “Mfumu Agripa, ndi onse amene
muli nafe pano, mukumuona munthu uyu! Ayuda onse anandipempha
ine za uyu ku Yerusalemu ndiponso kuno ku Kaisareya, mofuwula kuti,
ameneyu sayenera kukhala ndi moyo. 25 Ine ndinapeza kuti iyeyu
sanachite kanthu koyenera kufa, koma popeza anapempha kuti apite
kwa mfumu ya Chiroma, ine ndinatsimikiza zomutumiza ku Roma.
26 Koma ndilibe kanthu kenikeni koti ndilembere Wolemekezekayo za
iyeyu. N’chifukwa chake ndabwera naye pamaso pa nonsenu, makamaka
kwa inuyo mfumu Agripa, kuti mwina mukamufunsitsa ndikhale ndi choti
ndilembe. 27 Pakuti ine ndikuganiza kuti ndi chinthu chopanda nzeru
kutumiza wam’ndende popanda kutchula zifukwa zenizeni za mlandu
wake.”

# 26

### *Mawu a Paulo Pamaso pa Mfumu Agripa*

1 Ndipo Agripa anawuza Paulo kuti, “Takulola kuti unene mawu ako.”
Paulo anatambasula dzanja lake nayamba kudziteteza kuti, 2 “Mfumu
Agripa ine ndikudziyesa wa mwayi kuyima pamaso panu lero lino ndi
kudziteteza, kutsutsa zonse zimene Ayuda andinenera, 3 ndipo makamaka
chifukwa inu mukudziwa bwino miyambo yonse ya Chiyuda ndiponso
zonse zimene amatsutsana. N’chifukwa chake ndikukupemphani kuti
mundimvetsere moleza mtima.

4 “Ayuda onse akudziwa za moyo wanga mmene ndakhalira kuyambira
ndili mwana, kuchokera pachiyambi cha moyo wanga m’dziko lathu
ndiponso mu Yerusalemu. 5 Iwo akundidziwa kuyambira kalekale ndipo
angathe kuchitira umboni kuti ndakhala ndili Mfarisi moyo wanga wonse,
mmodzi wa gulu limene limasamala chipembedzo chathu koposa. 6 Ndipo
tsopano ndikuyimbidwa mlandu lero chifukwa cha chiyembekezo changa
pa zimene Mulungu analonjeza makolo athu. 7 Ili ndi lonjezo limene
mafuko athu khumi ndi awiri akuyembekezera kuti likwaniritsidwe
pamene akupembedza Mulungu molimbika usana ndi usiku. Wole-
mekezeka Mfumu, n’chifukwa cha chiyembekezo chimenechi Ayuda kuti
akundiyimba mlandu. 8 N’chifukwa chiyani ena a inu mukuganiza kuti
n’kosatheka kuti Mulungu aukitse akufa?

9 “Inenso ndimaganiza kuti ndimayenera kuchita zinthu zambiri pofuna
kuthana ndi dzina la Yesu wa ku Nazareti. 10 Ndipo izi ndi zimene
ndinazichita ku Yerusalemu. Ndi ulamuliro wa akulu a ansembe, ine
ndinayika m’ndende oyera mtima ambiri, ndipo pamene amaphedwa,
ine ndimavomereza. 11 Nthawi zambiri ndinkapita m’sunagoge iliyonse
kuti alangidwe, ndipo ndinayesera kuwakakamiza kuti achitire chipongwe
Mulungu. Mu mkwiyo wangawo, ndimapita ngakhale ku mizinda
yachilendo kuti ndikawazunze.

12 “Pa ulendo wina wotere, ndikupita ku Damasiko ndi mphamvu ndi
ulamuliro ochokera kwa akulu a ansembe, 13 Wolemekezeka Mfumu,
nthawi ya masana pamene ndimayenda pa msewu, ndinaona kuwala
kuchokera kumwamba koposa kuwala kwa dzuwa kutandizungulira ine
pamodzi ndi anzangawo. 14 Tonse tinagwa pansi ndipo ndinamva
mawu m’Chihebri akuti, ‘Saulo, Saulo chifukwa chiyani ukundizunza Ine?
N’kovuta kulimbikira mtunda wopanda madzi.’ ”

15 Ndipo ine ndinafunsa kuti, “Ndinu ndani Ambuye?”

Ambuye anayankha kuti, "Ndine Yesu, amene iwe ukumuzunza.
16 Tsopano dzuka ndipo imirira. Ine ndaonekera kwa iwe kuti ndikusankhe kuti ukhale mtumiki ndiponso mboni ya zimene waziona za Ine ndiponso zimene ndidzakuonetsa.
17 Ine ndidzakulanditsa m'manja mwa anthu a mtundu wako ndiponso mwa anthu a mitundu ina. Ine ndikukutuma kwa iwo,
18 kuti ukatsekule maso awo kuti atembenuke mtima kuchoka ku mdima ndi kulowa m'kuwala, kuchoka ku mphamvu za Satana ndi kupita kwa Mulungu, kuti alandire chikhululukiro cha machimo awo ndi kukhala m'gulu la amene akuyeretsedwa chifukwa chokhulupirira Ine.

19 "N'chifukwa chake Mfumu Agripa, sindinakane kumvera masomphenya wochokera kumwamba.
20 Kuyambira kwa anthu a ku Damasiko, a ku Yerusalemu, a ku Yudeya konse ndi kwa anthu a mitundu inanso, ndinalalikira kuti akuyenera kulapa ndi kutembenukira kwa Mulungu ndikuti aonetse kulapa kwawo mwa ntchito zawo.
21 Ichi n'chifukwa chake Ayuda anandigwira m'bwalo la Nyumba ya Mulungu nafuna kundipha.
22 Koma Mulungu wakhala akundithandiza mpaka lero lino. Ine ndayima pano kuti ndichitire umboni kwa anthu onse otchuka ndi anthu wamba. Ine sindikunena zina zowonjezera koma zimene Aneneri ndi Mose ananena kuti zidzachitika.
23 Iwo ananena kuti Khristu adzamva zowawa ndipo popeza Iye adzakhala woyamba kuuka kwa akufa, adzalalikira za kuwunika kwa anthu a mtundu wake ndiponso kwa anthu a mitundu ina."

24 Paulo akudziteteza, Festo anakweza mawu nati, "Wazungulira mutu Paulo! Kuphunzira kwako kwakuchititsa misala."

25 Paulo anayankha nati, "Wolemekezeka Festo, sindine wozungulira mutu. Zimene ndikunena ndi zoona ndiponso za nzeru.
26 Mfumu ikuzidziwa bwino zinthu izi, ndipo ndikuyankhula momasuka kwa iyo. Ine ndikukhulupirira kuti palibe kanthu n'kamodzi komwe kamene sukukadziwa, chifukwa izi sizinachike mseri.
27 Mfumu Agripa, kodi mumakhulupirira mawu a aneneri? Ine ndikudziwa kuti mumakhulupirira."

28 Kenaka Agripa anati kwa Paulo, "Kodi ukuganiza kuti m'kanthawi kochepa kotere ungandikope kuti ndikhale Mkhristu?"

29 Paulo anayankha kuti, "Ngakhale kanthawi kochepa kapena nthawi yayitali, ine ndikupempha kwa Mulungu kuti osati inu nokha koma aliyense amene akundimva lero lino akhale monga ine, kupatulapo maunyolo okhawa."

30 Mfumu inayimirira pamodzi ndi bwanamkubwa ndi Bernisi ndiponso anthu onse amene anakhala nawo pamodzi.
31 Inatuluka m'chipindamo, ndipo pamene imayankhula inati, "Munthu uyu sanachite kanthu koyenera kuphedwa kapena kumangidwa."

32 Agripa anati kwa Festo, "Munthu uyu akanamasulidwa akanakhala kuti sanapemphe zokaonekera kwa Kaisara."

# 27

*Paulo Apita ku Roma*

1 Zitatsimikizika kuti tiyenera kupita ku Italiya pa sitima ya pa madzi, anamupereka Paulo pamodzi ndi a m'ndende ena kwa msilikali wolamulira asilikali 100, dzina lake Yuliyo, amene anali wa gulu la asilikali lotchedwa, Gulu la Mfumu.
2 Tinakwera sitima ya pamadzi yochokera ku Adramutiyo imene inali yokonzeka kale kupita ku madooko a ku Asiya,

ndipo tinanyamuka. Aristariko, wa ku Makedoniya wa ku mzinda wa
Tesalonika, anali nafe.

3 Mmawa mwake tinafika ku Sidoni; ndipo Yuliyo, mokomera mtima
Paulo, anamulola kupita kwa abwenzi ake kuti akamupatse zosowa
zake. 4 Kuchokera kumeneko tinayambanso ulendo pa nyanja ndipo
tinadutsa kumpoto kwa chilumba cha Kupro chifukwa mphepo ima-
womba kuchokera kumene ife timapita. 5 Titawoloka nyanja mbali
ya gombe la Kilikiya ndi Pamfiliya, tinakafika ku Mura, mzinda wa
ku Lukia. 6 Kumeneko wolamulira asilikali 100 uja anapeza sitima ya
pamadzi ya ku Alekisandriya imene imapita ku Italiya, ndipo anatikweza
m'menemo. 7 Tinayenda pang'onopang'ono kwa masiku ambiri ndipo
tinakafika kufupi ndi Knido movutikira. Pamene mphepo sinatilole
kupitirira ulendo wathu molunjika, tinadzera kummwera kwa chilumba
cha Krete, moyang'anana ndi Salimoni. 8 Timayenda movutikira m'mbali
mwa chilumbacho ndipo tinafika pa malo wotchedwa Madooko Okoma,
pafupi ndi mzinda wa Laseya.

9 Tinataya nthawi yayitali, ndipo kuyenda pa nyanja kunali koopsa
chifukwa n'kuti tsopano nthawi yosala kudya itapita kale. Choncho Paulo
anawachenjeza kuti, 10 "Anthu inu, ine ndikuona kuti ulendo wathuwu
ukhala woopsa ndipo katundu ndi sitima ziwonongeka, ngakhalenso
miyoyo yathu." 11 Koma wolamulira asilikali 100 uja, m'malo momvera
zimene Paulo amanena, anatsatira malangizo a woyendetsa sitimayo
ndiponso mwini wa sitimayo. 12 Popeza kuti dookolo silinali labwino
kukhalako nthawi yozizira anthu ambiri anaganiza kuti tichoke. Ife
tinkayembekeza kukafika ku Foinikisi ndi kukhala kumeneko nthawi
yachisanu. Ili linali dooko la ku Krete, limene limaloza kummwera cha
kumadzulo ndiponso kumpoto cha kumadzulo.

### *Namondwe pa Nyanja*

13 Mphepo yochokera kummwera itayamba kuwomba
pang'onopang'ono, anthuwo anaganiza kuti apeza chimene amafuna;
kotero analowetsa nangula ndipo anayamba kuyenda m'mbali mwa
chilumba cha Krete. 14 Pasanathe nthawi yayitali, mphepo yamkuntho
yotchedwa Eurokulo, inayamba kuwomba kuchokera ku chilumbacho.
15 Mphepo yamkunthoyo inawomba sitima ija ndipo sinathe kulimbana
nayo, kotero ife tinayigonjera ndi kuyamba kutengedwa nayo. 16 Tikudutsa
m'mbali mwa kachilumba kakang'ono kotchedwa Kawuda, tinavutika
kuti tisunge bwato lopulumukiramo. 17 Anthuwo atakweza bwatolo
m'sitima, anakulunga zingwe sitimayo kuti ayilimbitse. Poopa kuti
angakagunde mchenga wa ku Surti, iwo anatsitsa nangula ndi kuyilola
sitima kuti idzingoyenda ndi mphepo. 18 Ife tinavutika kwambiri ndi
namondwe kotero kuti mmawa mwake tinayamba kuponya katundu
m'madzi. 19 Pa tsiku lachitatu anaponya m'nyanja zipangizo za m'sitima
ndi manja awo. 20 Sitinaone dzuwa kapena nyenyezi kwa masiku ambiri
ndipo namondwe anapitirira kuwomba kwambiri, pomaliza ife tonse
tinalibenso chiyembekezo choti n'kupulumuka.

21 Anthu aja atakhala nthawi yayitali osadya, Paulo anayimirira pakati
pawo ndipo anati, "Anthu inu, mukanamvera malangizo anga oti ti-
sachoke ku Krete: zonsezi sizikanawonongeka ndi kutayika. 22 Koma
tsopano ndikuti limbani mtima, chifukwa palibe aliyense wa inu amene
adzataya moyo wake; koma sitima yokhayi idzawonongeka. 23 Usiku

wathawu mngelo wa Mulungu, Mulungu amene ine ndili wake ndipo
ndimamutumikira, anayima pafupi ndi ine, 24 ndipo iyeyu anati, ‘Usachite
mantha, Paulo. Ukuyenera kukayima pamaso pa Kaisara; ndipo Mulungu
mwa kukoma mtima kwake wakupatsa miyoyo ya anthu onse amene
ukuyenda nawo.’ 25 Tsono limbani mtima, anthu inu, pakuti ine ndili ndi
chikhulupiriro mwa Mulungu kuti zichitika monga momwe wandiwuzira.
26 Komabe tiyenera kukatsakamira pa chilumba china chake.”

### *Kuwonongeka kwa Sitima*

27 Pakati pa usiku wa tsiku la khumi ndi chinayi tikukankhidwabe
ndi mphepo m’nyanja ya Adriya, oyendetsa sitimayo anazindikira kuti
timayandikira ku mtunda. 28 Iwo anatenga choyezera kuzama kwa nyanja
ndi kupeza kuti kuzama kwake kunali mamita 36. Atayendanso pang’ono
anatenganso choyezera chija napeza kuti kuzama kwake kunali 27.
29 Poopa kuti tingagunde miyala, iwo anatsitsira anangula anayi m’madzi
kumbuyo kwa sitimayo ndipo tinapemphera kuti kuche. 30 Pofuna
kuthawa m’sitimayo, oyendetsa aja anatsitsira m’nyanja bwato lopulu-
mukiramo n’kumachita ngati akufuna kutsitsira anangula m’nyanjamo
kutsogolo kwa sitimayo. 31 Pamenepo Paulo anawuza wolamulira asilikali
uja ndi asilikaliwo kuti, “Ngati anthu awa sakhala m’sitima muno, inu
simungapulumuke.” 32 Pamenepo asilikaliwo anadula zingwe za bwatolo
ndipo linagwera m’madzi.

33 Kutatsala pang’ono kucha, Paulo anawawumiriza anthu onse kuti
adye. Iye anati, “Kwa masiku khumi ndi anayi mwakhala mukuda nkhawa
ndipo simumadya kanthu kalikonse. 34 Tsopano ine ndikukupemphani
kuti mudye. Muyenera kudya kuti mupulumuke. Palibe ndi mmodzi
yemwe wa inu adzataye ngakhale tsitsi limodzi la pamutu pake.” 35 Paulo
atanena zimenezi, anatenga buledi nayamika Mulungu pamaso pa onse.
Ndipo ananyema bulediyo nayamba kudya. 36 Onse analimba mtima
nayamba kudyanso. 37 Tonse pamodzi m’sitimamo tinalipo anthu 276.
38 Onse atadya, nakhuta anapeputsa sitimayo potaya tirigu m’nyanja.

39 Kutacha, anthu sanazindikire dzikolo, koma anaona pomwe sitima
zimayimapo pamodzi ndi mchenga wa pa gombe. Iwo anaganiza
zokocheza sitimayo kumeneko ngati zikanatheka kutero. 40 Atadula
anangula aja, nawasiya m’nyanja, pa nthawi yomweyo anamasula zingwe
zimene anamangira zowongolera sitimayo. Kenaka anayimika chinsalu
chimene mphepo imakankha kuti sitima iyende, ndipo anayamba kupita
ku gombe. 41 Koma sitimayo inagunda mchenga wobisika ndipo inayima.
Mbali ya kutsogolo ya sitimayo inakanirira ndipo sinathe kuyendanso,
ndipo mbali yakumbuyo inasweka ndi kuwomba kwa mafunde.

42 Asilikali anaganiza za kupha am’ndende onse, kuti angasambire
kupita pa mtunda ndi kuthawa. 43 Koma wolamulira asilikali uja
anafuna kupulumutsa Paulo ndipo anawaletsa kuchita zimene anakonza.
Iye analamulira asilikali kuti amene amatha kusambira kuti adziponye
m’madzi ndi kuyamba kukafika pa mtunda. 44 Otsalawo anayenera kug-
wira matabwa kapena tizidutswa ta sitimayo. Motero onse anapulumuka
nakafika pa mtunda.

# 28

### *Paulo pa Chilumba cha Melita*

1 Titapulumuka choncho, tinamva kuti chilumbacho chimatchedwa
Melita. 2 Anthu a pa chilumbacho anatichitira zokoma zimene sizichitika
kawirikawiri. Iwo anakoleza moto natilandira tonse chifukwa kumagwa
mvula ndipo kumazizira. 3 Paulo anatola mtolo wankhuni, pamene
amayika pa moto, munatulukamo njoka chifukwa cha kutentha, ndipo
inamuluma pa dzanja. 4 Anthu a pa chilumbacho ataona njokayo ili lende
pa dzanja lake, iwo anawuzana kuti, "Munthu uyu akuyenera kukhala
munthu wopha anthu; pakuti ngakhale wapulumuka pa nyanja, chilung-
amo sichinamulore kuti akhale ndi moyo." 5 Koma Paulo anayikutumulira
pa moto njokayo, ndipo sanamve kupweteka. 6 Anthu anayembekezera
kuti thupi lake litupa kapena agwa ndi kufa mwadzidzidzi, koma anadikira
nthawi yayitali. Ataona kuti palibe kanthu kachilendo kanamuchitikira
anasintha maganizo awo nanena kuti iye ndi mulungu.

7 Pafupi ndi malowa panali munda wa Popliyo, mkulu wa boma la pa
chilumbacho. Iye anatilandira natisamala bwino masiku atatu. 8 Abambo
ake anali gone, chifukwa amadwala malungo ndi kamwazi. Paulo analowa
m'chipinda chake kukawaona, ndipo atapemphera, anasanjika manja ake
pa iwo nawachiritsa. 9 Zitachitika zimenezi, anthu onse odwala a pa
chilumbacho anabwera ndipo anachiritsidwa. 10 Anthuwo anatilemekeza
ife m'njira zambiri ndipo pamene tinakonzeka kuti tiyambe ulendo,
anatipatsa zonse zomwe tinazisowa.

### *Paulo Afika ku Roma*

11 Patapita miyezi itatu, tinanyamuka pa sitima ina imene inakhala pa
chilumbacho chifukwa cha kuzizira. Inali sitima ya ku Alekisandriya
imene inali ndi chizindikiro cha milungu ya mapasa yotchedwa Kastro ndi
Polikisi. 12 Tinakafika ku Surakusa ndipo kumeneko tinakhalako masiku
atatu. 13 Kuchokera kumeneko tinayenda ndi kukafika ku Regio. Mmawa
mwake mphepo yochokera kummwera inawomba, ndipo tsiku linalo
tinakafika ku Potiyolo. 14 Kumeneko tinapezako abale amene anatiyitana
kuti tikhale nawo sabata limodzi. Ndipo kenaka tinapita ku Roma. 15 Abale
kumeneko atamva kuti tikubwera, anabwera kudzakumana nafe mpaka
ku bwalo la Apiyo ndiponso ku nyumba za alendo zitatu. Atawaona anthu
amenewa Paulo anayamika Mulungu ndipo analimbikitsidwa. 16 Titafika
ku Roma, Paulo analoledwa kukhala pa yekha ndi msilikali womulondera.

### *Paulo Alalikira kwa Ayuda ku Roma*

17 Patapita masiku atatu, Paulo anasonkhanitsa pamodzi atsogoleri a
Ayuda. Atasonkhana, Paulo anawawuza kuti, "Abale anga, ngakhale
kuti ine sindinachite kanthu kalikonse kulakwira mtundu wathu kapena
miyambo ya makolo athu, koma anandigwira mu Yerusalemu ndi
kundipereka m'manja mwa Aroma. 18 Iwo anandifufuza ndipo ana-
funa kundimasula chifukwa sanandipeze wopalamula mlandu woyenera
kuphedwa. 19 Koma Ayuda atakana, ine ndinakakamizidwa kupempha
kuti ndikaonekere pamaso pa Kaisara, sikuti ndinali ndi kanthu konenez-
era mtundu wanga. 20 Pa chifukwa ichi ndapempha kuti ndionane nanu
ndi kuyankhula nanu. Pakuti n'chifukwa cha chiyembekezo cha Israeli
ndamangidwa unyolo uwu."

21 Iwo anayankha kuti, "Ife sitinalandire kalata iliyonse yochokera ku
Yudeya yonena za iwe, ndipo palibe mmodzi wa abale amene anachokera
kumeneko anafotokoza kapena kunena kalikonse koyipa ka iwe. 22 Koma

ife tikufuna kumva maganizo ako ndi otani, pakuti tikudziwa kuti
ponseponse anthu akuyankhula zotsutsana ndi mpatuko umenewu.”
23 Iwo anakonza tsiku lina loti akumane ndi Paulo, ndipo anabwera
anthu ambiri ku nyumba kumene amakhala. Kuyambira mmawa mpaka
madzulo, Paulo anawafotokozera ndi kuwawuza za ufumu wa Mulungu
ndipo anayesa kuwakopa kuti akhulupirire Yesu kuchokera m’Malamulo a
Mose ndiponso m’mabuku a Aneneri. 24 Ena anakopeka ndi zimene Paulo
ananena, koma enanso sanakhulupirire. 25 Ndipo anayamba kuchoka
popeza sanagwirizane pakati pawo Paulo atanena mawu awa omaliza
akuti, “Mzimu Woyera anayankhula zoona za makolo anu pamene Iye
ananena kudzera mwa Mneneri Yesaya kuti,

26 “Pita kwa anthu awa ndi kuwawuza kuti,
‘Kumva mudzamva, koma osamvetsetsa;
kupenya mudzapenya, koma osaona kanthu.’
27 Pakuti mtima wa anthu ndi wokanika;
m’makutu mwawo ndi mogontha,
ndipo atsinzina kuti asaone kanthu.
Mwina angapenye ndi maso awo,
angamve ndi makutu awo,
angamvetse ndi nzeru zawo ndi kutembenuka,
Ineyo n’kuwachiritsa.

28 “Chifukwa chake ine ndikufuna mudziwe kuti chipulumutso cha
Mulungu chatumizidwa kwa anthu a mitundu ina, ndipo iwo adzamvera.”
29 Paulo atanena mawu amenewa, Ayuda aja anachoka akutsutsana
kwambiri.
30 Paulo anakhala kumeneko zaka ziwiri zathunthu m’nyumba yobw-
ereka yomwe amalipira ndipo ankalandira aliyense amene amabwera
kudzamuona. 31 Molimba mtima ndi popanda womuletsa, Paulo anala-
likira za ufumu wa Mulungu ndi kuphunzitsa za Ambuye Yesu Khristu.

# KALATA YA PAULO YOLEMBERA AROMA

1 Ndine Paulo, mtumiki wa Khristu Yesu, woyitanidwa ndi Mulungu
kukhala mtumwi. Ndinapatulidwa kuti ndilalikire Uthenga Wabwino
wa Mulungu 2 umene analonjeza kale m’Malemba Oyera kudzera mwa
aneneri ake. 3 Uthengawu ndi wonena za Mwana wake amene mwa
umunthu wake anali wochokera mwa Davide. 4 Iyeyu ndi amene
anatsimikizidwa kukhala Mwana wa Mulungu mwamphamvu za Mzimu
Woyera pamene anauka kwa akufa. Kudzera mwa Ambuye athu Yesu
Khristu, 5 ife tinalandira chisomo chokhala atumwi oyitana anthu a
mitundu yonse kuti amukhulupirire ndi kumumvera mwachikhulupiriro
kuti dzina lake lilemekezedwe. 6 Inunso muli m’gulu la Amitundu
oyitanidwawo kukhala ake a Yesu Khristu.

7 Ndikulembera kwa onse okhala ku Roma amene Mulungu amakukondani nakuyitanani kuti mukhale oyera mtima.

Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate athu ndi kwa Ambuye Yesu Khristu zikhale ndi inu.

### *Paulo Afunitsitsa Kukacheza ku Roma*

8 Poyamba, ndikuthokoza Mulungu wanga kudzera mwa Yesu Khristu
chifukwa cha nonsenu, pakuti pa dziko lonse lapansi anthu akukamba
za chikhulupiriro chanu. 9 Mulungu amene ndimamutumikira ndi mtima
wanga onse polalikira Uthenga Wabwino wa Mwana wake, ndi mboni
yanga kuti ndimakupemphererani nthawi zonse. 10 M’mapemphero anga,
nthawi zonse, ndimapemphera kuti ngati n’kotheka mwachifuniro cha
Mulungu, njira inditsekukire kuti ndibwere kwanuko.

11 Ine ndikulakalaka kukuonani kuti ndikugawireni mphatso zina
zauzimu kuti zikulimbikitseni 12 ndiponso kuti tonsefe tilimbikitsane
m’chikhulupiriro wina ndi mnzake. 13 Abale, ine sindifuna kuti mukhale
osadziwa kuti nthawi zambiri ndakhala ndikufuna zobwera kwanuko,
koma mpaka pano pali zolepheretsa, ndi cholinga choti ndidzapezeko
zipatso pakati panupo monga momwe ndakhala ndikuchitira pakati pa
a mitundu ina.

14 Ine ndi wokakamizidwa ndi udindo wotumikira Agriki pamodzi ndi
omwe si Agriki, kwa anzeru ndi kwa opusa omwe. 15 Pa chifukwa
chimenechi, ine ndikufunitsitsa kulalikira Uthenga Wabwino kwa inunso
amene muli ku Roma.

16 Ine sindichita manyazi ndi Uthenga Wabwino chifukwa ndiwo
mphamvu za Mulungu zopulumutsa aliyense amene akhulupirira,
poyamba Myuda, kenaka Mhelene. 17 Pakuti mu Uthenga
Wabwino anawulula kuti chilungamo chimachokera kwa Mulungu.
Kuyambira pachiyambi mpaka potsiriza ndi chilungamo chobwera
mwachikhulupiriro, monga kwalembedwera kuti, “Wolungama adzakhala
ndi moyo mwachikhulupiriro.”

### *Mkwiyo wa Mulungu pa Mtundu wa Anthu*

18 Mkwiyo wa Mulungu ukuonekera kuchokera kumwamba. Ukutsutsana ndi kusapembedza konse ndi kuyipa kwa anthu amene amapondereza choonadi mwa chikhalidwe chawo choyipa. 
19 Za Mulungu

zimene zingathe kudziwika, ndi zomveka bwino kwa iwo pakuti Mulungu
anazionetsera kwa iwo. 20 Pakuti kuyambira pamene dziko lapansi
linalengedwa, zinthu zosaoneka za Mulungu, mphamvu zake zosatha
ndi chikhalidwe cha umulungu, zakhala zikuoneka bwinobwino. Akhala
akuzindikira poona zimene Mulungu analenga, kotero kuti anthu sangathe
kuwiringula.

21 Ngakhale iwo anadziwa Mulungu, sanamulemekeze ngati Mulungu
kapena kumuthokoza, koma maganizo awo anasanduka wopanda pake
ndipo m'mitima yawo yopusa munadzaza mdima. 22 Ngakhale ankadzi-
tama kuti ndi anzeru, anasanduka opusa. 23 Iwo anasinthanitsa ulemerero
wa Mulungu wosafa ndi mafano opangidwa ndi manja wooneka ngati
munthu amene amafa, kapena ngati mbalame, ndi nyama kapena
zokwawa.

24 N'chifukwa chake Mulungu anawasiya kuti azingochita zilakolako
zochititsa manyazi zauchimo zomwe mitima yawo inkafuna. Zotsatira
zake anachita za chiwerewere wina ndi mnzake kunyazitsa matupi
awo. 25 Iwo anasinthanitsa choonadi cha Mulungu ndi bodza ndipo
anapembedza ndi kutumikira zinthu zolengedwa m'malo mwa Mlengi
amene ali woyenera kutamandidwa mpaka muyaya. Ameni.

26 Chifukwa cha ichi, Mulungu anawasiya kuti azitsata zilakolako
zochititsa manyazi. Ngakhale akazi omwe anasiya machitidwe achibad-
widwe pa za ukwati, namachita machitidwe ena otsutsana ndi chibadwa
chawo. 27 Chimodzimodzinso amuna analeka machitidwe a ukwati ndi
akazi n'kumakhumbana amuna okhaokha. Amuna ankachita zochitisa
manyazizi ndi amuna anzawo, ndipo analandira chilango choyenera
molingana ndi zochita zawo zachitayikozo.

28 Ndipo popeza anaona kuti n'chopanda nzeru kumvera Mulungu,
Iye anawasiya kuti atsatire maganizo achitayiko kuti achite zosayenera
kuchitazo. 29 Iwo ndi odzazidwa ndi mtundu uliwonse wa makhalidwe
oyipa, zonyansa, umbombo ndi dumbo. Iwo ndi odzazidwa ndi
kaduka, kupha, mikangano, chinyengo ndi udani. Iwowo ndi amiseche,
30 osinjirira, odana ndi Mulungu, achipongwe, odzitama ndi odzitukumula.
Iwo amapeza njira zochitira zoyipa. Samvera makolo awo, 31 alibe
nzeru, chikhulupiriro, sakhudzidwa mu mtima ndipo ndi ankhanza.
32 Ngakhale kuti amadziwa chiweruzo cholungama cha Mulungu chakuti
amene amachita zinthu zotere amayenera imfa, iwo sangopitiriza chabe
zimenezi, koma amavomerezanso amene amazichita zimenezi.

# 2

### *Kuweruza Kolungama kwa Mulungu*

1 Choncho, iwe amene umaweruza munthu wina, ulibe pokanira pakuti
nthawi iliyonse pamene uweruza wina ukudzitsutsa wekha chifukwa
iwe amene umaweruzawe umachitanso zinthu zomwezo. 2 Tsopano ife
tikudziwa kuti chiweruzo cha Mulungu, chotsutsa amene amachita zinthu
zotere, n'chokhazikika pa choonadi. 3 Kodi ukuganiza kuti udzathawa
chiweruzo cha Mulungu iwe munthu wamba, pamene uweruza ena,
iwe ndi kumachitanso zomwezo? 4 Kodi kapena ukupeputsa kukoma
mtima kwa Mulungu, kuleza mtima kwake ndi kupirira kwake? Kodi
sukuzindikira kuti kukoma mtima kwakeko, n'kofuna kuti iweyo ulape
machimo ako?

5 Koma pakuti ndiwe wosamvera ndi wa mtima wosafuna kulapa,
ukudzisungira chilango pa tsiku la mkwiyo wa Mulungu, pamene chi-
weruzo cholungama cha Mulungu chidzaonetsedwa. 6 Mulungu adzab-
wezera aliyense molingana ndi ntchito zake. 7 Iye adzapereka moyo
wosatha kwa amene amafunafuna ulemerero, ulemu ndi moyo pochita
ntchito zabwino mopirira. 8 Koma Mulungu adzakhuthulira mkwiyo
ndi ukali wake pa amene amachita zofuna zawo ndi kukana choonadi
n'kumatsatira zoyipa. 9 Masautso ndi zowawa zidzagwera munthu
aliyense amene amachita zonyansa, kuyambira Myuda kenaka anthu a
mitundu ina. 10 Koma ulemerero, ulemu ndi mtendere zidzakhala kwa
aliyense amene amachita zabwino, kuyambira Myuda kenaka anthu a
mitundu ina. 11 Pajatu Mulungu alibe tsankho.

12 Onse amene amachimwa osadziwa Malamulo, adzawonongeka
ngakhale kuti sadziwa Malamulowo. Ndipo onse amene amachimwa
akudziwa Malamulo adzaweruzidwa potsata Malamulowo. 13 Pakuti
si amene amangomva Malamulo amene amakhala wolungama pamaso
pa Mulungu, koma ndi okhawo amene amachita zili m'Malamulomo
amene adzatchedwa olungama. 14 Ndithu, pamene a mitundu ina, amene
alibe Malamulo, koma mwachikhalidwe chawo amachita zimene zili
m'Malamulo, iwowo ndi Malamulo pa iwo okha, ngakhale kuti alibe
Malamulowo. 15 Ntchito zawo zimaonetsa kuti Malamulowo alembedwa
m'mitima mwawo. Chikumbumtima chawonso chimawachitira umboni
pakuti maganizo awo amawatsutsa kapena kuwavomereza. 16 Izi zidza-
chitika pa tsiku limene Mulungu adzaweruza zinsinsi za anthu kudzera
mwa Yesu Khristu, monga momwe Uthenga wanga Wabwino unenera.

### *Ayuda ndi Malamulo*

17 Koma iweyo, amene umadzitcha kuti ndiwe Myuda, umadalira
Malamulo, ndipo umanyadira ubale wako ndi Mulungu, 18 ngati umadziwa
chifuniro chake, ndi kudziwa zoyenera kuchita chifukwa unaphunzit-
sidwa ndi Malamulo; 19 ngati umadziwadi kuti ndiwe mtsogoleri wa
osaona, nyale yowunikira amene ali mu mdima, 20 mlangizi wa anthu
opusa, mphunzitsi wa makanda, chifukwa umadziwa kuti m'Malamulo
uli nayo nzeru yonse ndi choonadi, 21 tsono, iwe amene umaphunzitsa
ena, sudziphunzitsa wekha kodi? Kodi iwe amene umalalikira kuti anthu
asabe, umabanso? 22 Kodi iwe amene umanena kuti anthu asachite
chigololo, umachitanso chigololo? Kodi iwe amene umanyasidwa ndi
mafano, umalandanso za m'nyumba zopembedzera mafanowo? 23 Kodi
iwe amene umadzitama ndi Malamulo, umamuchititsa manyazi Mulungu
posamvera Malamulowo? 24 Monga kwalembedwa, "Dzina la Mulungu
likuchitidwa chipongwe pakati pa a mitundu ina chifukwa cha inu."

25 Mdulidwe umakhala ndi phindu ngati usunga Malamulo, koma ngati
sumvera Malamulo, iweyo umakhala ngati kuti sunachite mdulidwe.
26 Ngati amene sanachite mdulidwe achita zomwe zili m'Malamulo,
kodi sadzatengedwa ngati ochita mdulidwe? 27 Munthu amene sana-
chite mdulidwe m'thupi koma amamvera Malamulo adzakutsutsa iwe
wosamvera Malamulowe, ngakhale kuti uli nawo Malamulo olembed-
wawo.

28 Myuda weniweni si amene angooneka ngati Myuda pamaso pa anthu,
ndipo mdulidwe weniweni si umene umangochitika m'thupi pamaso pa
anthu. 29 Ayi, Myuda weniweni ndi amene ali Myuda mu mtima mwake,

ndipo mdulidwe weniweni ndi wa mtima, wochitika ndi Mzimu, osati ndi
malamulo olembedwa. Woyamikira munthu wotere ndi Mulungu, osati
anthu ayi.

# 3

*Kukhulupirika kwa Mulungu*

1 Nanga kodi pali ubwino wotani pokhala Myuda, kapena muli ubwino
wanjinso mu mdulidwe? 2 Ubwino wake ndi wambiri m'njira zonse!
Choyambirira iwo anapatsidwa Mawu a Mulungu kuti awasunge.
3 Nanga zili bwanji ngati ena analibe chikhulupiriro? Kodi kupanda
chikhulupiriro kwawo kukanalepheretsa kukhulupirika kwa Mulungu?
4 Ayi. M'njira iliyonse ayi! Mulungu akhale woona, ndi munthu aliyense
akhale wonama. Monga kwalembedwa kuti,
"Kotero kuti inu mwapezeka kuti ndinu wolungama pamene muyankhula
ndi kupambana pamene muweruza."
5 Koma ngati kuyipa mtima kwathu kuonetsa poyera kuti Mulungu ndi
wolungama, ife tinganene chiyani? Kodi tinganene kuti Mulungu ndi
wosalungama pamene aonetsa mkwiyo wake pa ife? (Ine ndikuyankhula
monga mmene anthu ena amayankhulira). 6 Ayi. M'njira iliyonse
ayi! Ngati zikanakhala zotero, kodi Mulungu akanaweruza bwanji dziko
lapansi? 7 Wina atanena kuti, "Ngati kunama kwanga kukuonetsa
koposa kuti Mulungu ndi woona, ndi kuwonjezera pa ulemerero wake,
nanga n'chifukwa chiyani ndikuweruzidwa kuti ndine wochimwa?"
8 N'chifukwa chiyani osanena kuti, monga ena amanena mosasamala kuti,
"Tiyeni tichite zoyipa kuti zabwino zionekere?" Anthu onena zoterewa
kulangidwa kwawo ndi koyenera.

*Palibe Munthu Wolungama*

9 Kodi timalize bwanji? Kodi Ayuda ndife oposa anthu ena? Ayi. M'njira
iliyonse ayi! Ife tinanena kale kuti Ayuda ndi a mitundu ina omwe ndi
ochimwa. 10 Monga kwalembedwa kuti,
"Palibe munthu wolungama, inde palibe ndi mmodzi yemwe.
11 Palibe ndi mmodzi yemwe amene amazindikira,
palibe amene amafunafuna Mulungu.
12 Onse apatukira kumbali,
onse pamodzi asanduka opandapake.
Palibe ndi mmodzi yemwe amene amachita zabwino,
palibe ngakhale mmodzi."
13 "Kummero kwawo kuli ngati manda apululu;
ndi lilime lawo amayankhula zachinyengo."
"Ululu wa mamba uli pa milomo yawo."
14 "M'kamwa mwawo ndi modzaza ndi zotemberera ndi mawu
owawa."
15 "Mapazi awo afulumira kukakhetsa magazi.
16 Kusakaza ndi chisoni kumaonekera m'njira zawo,
17 ndipo njira ya mtendere sayidziwa."
18 "Saopa Mulungu ndi pang'ono pomwe."
19 Tsopano tikudziwa kuti chilichonse Malamulo amanena, amanena
kwa amene amalamulidwa ndi Malamulowo, ndi cholinga chakuti
aliyense asowe chonena, ndipo dziko lonse lidzayimbidwa mlandu ndi Mu-
lungu. 20 Chifukwa chake palibe mmodzi amene adzayesedwa wolungama

pamaso pake chifukwa chosunga Malamulo, kuti ife timazindikira tchimo kupyolera mu Malamulo.

### *Kulungama Mwachikhulupiriro*

21 Koma tsopano chilungamo chochokera kwa Mulungu, osati chochok-
era ku Malamulo, chaonetsedwa. Ichi ndi chimene Malamulo ndi Aneneri
amachitira umboni. 22 Timakhala olungama pamaso pa Mulungu pamene
takhulupirira Yesu Khristu. Mulungu amachitira zimenezi anthu onse
amene akhulupirira Khristu. Palibe kusiyana pakati pa Myuda ndi a
mitundu ina, 23 pakuti onse anachimwa naperewera pa ulemerero wa
Mulungu 24 ndipo onse alungamitsidwa mwaulere mwa chisomo chake
chifukwa cha Khristu Yesu amene anawawombola. 25 Mulungu anamu-
pereka Iyeyu kuti pokhetsa magazi ake, akhale nsembe yokhululukira
machimo. Mulungu anachita zimenezi kufuna kuonetsa chilungamo
chake. Chifukwa cha kuleza mtima kwake, sanalange anthu chifukwa
cha machimo amene anachita kale. 26 Iye anachita izi kuti aonetse
chilungamo chake lero lino. Anthu azindikire kuti Iye ndi wolungama
ndipo amalungamitsa aliyense amene akhulupirira Yesu.

27 Nanga tsono pamenepa munthu anganyadenso? Kunyadatu kwa-
chotsedwa. Chifukwa cha Malamulo? Kodi Malamulo samafuna ntchito
za munthu? Ayi, koma mwachikhulupiriro. 28 Ife tikunenabe kuti munthu
amalungamitsidwa mwachikhulupiriro osati mwakusunga Malamulo.
29 Kodi Mulungu ndi Mulungu wa Ayuda okha? Kodi si Mulungu wa a mi-
tundu inanso? Inde wa a mitundu inanso, 30 popeza ndi Mulungu mmodzi
yemweyo amene adzalungamitsa mwachikhulupiriro ochita mdulidwe ndi
osachita mdulidwe kudzera m'chikhulupiriro chomwecho. 31 Kodi tsono
ife, tikutaya Malamulo pamene tikunena kuti pafunika chikhulupiriro?
Ayi. M'njira iliyonse ayi! Komatu ife tikukwaniritsadi Malamulo.

## 4

### *Abrahamu Analungamitsidwa Mwachikhulupiriro*

1 Nanga tsono tidzati chiyani za Abrahamu kholo lathu, iyeyu anapezana
ndi zotani pa nkhani imeneyi? 2 Kunena zoona, Abrahamu akanalungamit-
sidwa ndi ntchito zake, akanakhala nako kanthu kodzitamandira, koma
osati pamaso pa Mulungu. 3 Kodi Malemba akuti chiyani? "Abra-
hamu anakhulupirira Mulungu, ndipo ichi chinamuchititsa kukhala
wolungama."

4 Tsopano munthu amene wagwira ntchito, malipiro ake satengedwa
kukhala ngati mphatso koma zimene anayenera kulandira. 5 Koma kwa
munthu amene sanagwire ntchito ndipo akhulupirira Mulungu amene
amalungamitsa ochimwa, chikhulupiriro chakecho chimatengedwa
kukhala chilungamo. 6 Davide ponena zomwezi pamene anayankhula za
kudala kwa munthu amene Mulungu amulungamitsa osati chifukwa cha
ntchito zake akuti,

7 "Odala ndi amene
zoyipa zawo zakhululukidwa;
amene machimo awo afafanizidwa.
8 Ngodala munthu amene
machimo ake Ambuye sadzawakumbukiranso."

9 Kodi madalitso amenewa ali kwa ochita mdulidwe okha kapena kwa
amene sanachitepo mdulidwe? Ife takhala tikunena kuti chikhulupiriro

cha Abrahamu chinamuchititsa kukhala wolungama. [10] Kodi chi-
natengedwa bwanji? Kodi n'kuti iye atachita mdulidwe kapena asana-
chite? Osati atachita mdulidwe koma asanachite! [11] Ndipo iye anachita
mdulidwe ngati chizindikiro ndi chitsimikizo cha kulungama kumene
anali nako mwachikhulupiriro pomwe anali asanachite mdulidwe. Chon-
cho, iye ndi kholo la onse amene akhulupirira koma sanachite mdulidwe,
ndi cholinga chakuti alungamitsidwe. [12] Ndipo iyenso ndiyenso kholo la
ochita mdulidwe osati amene anangochita mdulidwe kokha koma amene
amatsata chitsanzo cha chikhulupiriro chimene kholo lathu Abrahamu
anali nacho asanachite mdulidwe.

[13] Abrahamu ndi zidzukulu zake sanalandire lonjezano lakuti adza-
landira dziko lapansi kudzera mu Malamulo, koma kudzera mu chilung-
amo chimene chimabwera ndi chikhulupiriro. [14] Pakuti ngati amene
amadalira Malamulo ndiye olowa m'malo, ndiye kuti chikhulupiriro
n'chopanda pake ndipo lonjezano ndi lopanda phindu [15] chifukwa Mala-
mulo anabweretsa chilango. Ndipo kumene kulibe Malamulo kulibenso
kuwalakwitsa.

[16] Motero, timalandira lonjezo mwachikhulupiriro. Laperekedwa
mwachisomo kuti patsimikizidwe kuti lonjezolo liperekedwa kwa ana ndi
zidzukulu zonse za Abrahamu, osati kwa iwo okha amene amatsatira
Malamulo komanso kwa iwo amene ali ndi chikhulupiriro cha Abrahamu.
Iye ndiye kholo la ife tonse. [17] Monga kwalembedwa kuti, "Ine ndakusan-
dutsa kukhala kholo la mitundu yambiri." Iye ndiye kholo lathu pamaso
pa Mulungu, amene anamukhulupirira, Mulungu amene amapereka moyo
kwa akufa ndipo amapereka moyo kwa zinthu zopanda moyo.

[18] Ngakhale zinali zosayembekezeka, Abrahamu anakhulupirira ndi
chiyembekezo kuti adzakhala kholo la mitundu yambiri. Izi ndi monga
zinanenedwa kwa iye kuti, "Ndi mmene adzakhalire ana ako ndi
zidzukulu zako." [19] Iye sanafowoke m'chikhulupiriro. Anadziwa choonadi
cha thupi lake kuti linali lakufa popeza anali ndi zaka pafupifupi 100
ndiponso mimba ya Sara inali yowuma. [20] Komabe iye sanagwedezeke
chifukwa chosakhulupirira pa zokhudzana ndi lonjezo la Mulungu. Iye
analimbikitsidwa m'chikhulupiriro chake ndi kupereka ulemerero kwa
Mulungu. [21] Anatsimikiza mu mtima mwake kuti Mulungu anali ndi
mphamvu yochita chomwe analonjeza. [22] N'chifukwa chake "chinamu-
chititsa kukhala wolungama." [23] Mawu akuti, "chinatengedwa kwa iye"
sanalembedwe chifukwa cha iye yekha, [24] komanso chifukwa ife amene
Mulungu adzatiyesa olungama, ife amene tikhulupirira mwa Iye amene
anamuukitsa kwa akufa, Yesu Ambuye athu. [25] Iye anaperekedwa kuti
aphedwe chifukwa cha machimo athu ndipo anaukitsidwa ndi kukhala
ndi moyo kuti tilungamitsidwe.

# 5

*Mtendere ndi Chimwemwe*

[1] Tsopano popeza tayesedwa olungama mwa chikhulupiriro, tili ndi
mtendere ndi Mulungu kudzera mwa Ambuye athu Yesu Khristu. [2] Iyeyo
ndiye amene anatsekulira njira mwachikhulupiriro yolowera m'chisomo
m'mene takhazikikamo. Ndipo tikukondwerera chiyembekezo cha ule-
merero wa Mulungu. [3] Koma si pokhapo ayi, koma ife tikukondweranso
m'masautso athu chifukwa tikudziwa kuti masautso amatiphunzitsa
kupirira. [4] Ndipo kupirira kumabweretsa makhalidwe, makhalidwe

amabweretsa chiyembekezo. [5] Ndipo chiyembekezo chimenechi sichi-
tikhumudwitsa chifukwa Mulungu mwa Mzimu Woyera, amene Iye
anatipatsa, wadzaza m'mitima mwathu ndi chikondi chake.

[6] Pakuti pa nthawi yake, tikanali ochimwa, Khristu anatifera anthu
osapembedzafe. [7] Sizichitika kawirikawiri kuti munthu wina afere
munthu wolungama, ngakhale kuti chifukwa cha munthu wabwino wina
atha kulimba mtima kumufera. [8] Koma Mulungu anaonetsa chikondi
chake kwa ife chifukwa pamene tinali ochimwabe, Khristu anatifera.

[9] Popeza chifukwa cha magazi ake ife tapezeka olungama pamaso pa
Mulungu, Iyeyo adzatipulumutsa koposa kotani ku mkwiyo wa Mulungu.
[10] Pakuti pamene tinali adani a Mulungu, tinayanjanitsidwa ndi Iye kudz-
era mu imfa ya Mwana wake. Nanga tidzapulumutsidwa bwanji kudzera
m'moyo wake, titayanjanitsidwa naye? [11] Sikuti izi zili chomwechi chabe,
koma timakondweranso mwa Mulungu kudzera mwa Ambuye athu Yesu
Khristu. Kudzera mwa Iye, ife tsopano tayanjanitsidwa ndi Mulungu.

### *Imfa Kudzera mwa Adamu, Moyo Kudzera mwa Yesu*

[12] Choncho monga momwe tchimo linalowa m'dziko lapansi kudzera
mwa munthu mmodzi, ndi imfa kudzera mu tchimo, m'njirayi imfa
inafika kwa anthu onse pakuti onse anachimwa. [13] Pakuti Malamulo
asanaperekedwe, tchimo linali m'dziko lapansi. Koma pamene palibe
Malamulo, tchimo silitengedwa kukhala tchimo. [14] Komabe, imfa inala-
mulira kuyambira nthawi ya Adamu mpaka nthawi ya Mose. Inalamulira
ngakhalenso pa iwo amene sanachimwe posamvera Malamulo monga
anachitira Adamu. Adamuyo amene anali chifaniziro cha wina amene
ankabwera.

[15] Koma sitingafananitse mphatso yaulereyo ndi kuchimwa kwa anthu.
Pakuti ngati anthu ambiri anafa chifukwa cha kuchimwa kwa munthu
mmodziyo, kuli koposa bwanji nanga chisomo cha Mulungu ndi mphatso
zomwe zinabwera ndi chisomo cha munthu mmodzi, Yesu Khristu, ndi
kusefukira kwa ambiri! [16] Ndiponso, mphatso ya Mulungu sifanana ndi
zotsatira za kuchimwa kwa munthu mmodzi. Chiweruzo chinatsatira
tchimo la munthu mmodzi ndi kubweretsa kutsutsidwa koma mphatso
inatsatira zolakwa zambiri ndi kubweretsa kulungamitsidwa. [17] Pakuti
ngati, chifukwa cha kulakwa kwa munthu mmodziyo, imfa inalamulira
kudzera mwa munthu mmodziyo, kuli koposa bwanji nanga kwa iwo
amene adzalandira chisomo chochuluka ndi mphatso yachilungamo,
adzalamulira m'moyo kudzera mwa munthu mmodzi, Yesu Khristu.

[18] Choncho monga tchimo limodzi linabweretsa kutsutsika pa anthu
onse, chimodzimodzinso ntchito imodzi yolungama inabweretsa chilung-
amo kwa anthu onse ndi kuwapatsa moyo. [19] Pakuti kusamvera
kwa munthu mmodzi kunasandutsa anthu ambiri kukhala ochimwa,
chimodzimodzinso anthu ambiri adzasanduka olungama kudzera mwa
munthu mmodzinso.

[20] Malamulo a Mulungu anaperekedwa ndi cholinga chakuti anthu
onse azindikire kuchuluka kwa machimo awo. Koma pamene machimo
anachuluka, chisomo chinachuluka koposa. [21] Choncho monga momwe
tchimo linkalamulira anthu ndi kubweretsa imfa pa iwo, chomwecho
kunali koyenera kuti chisomo chilamulire pobweretsa chilungamo kwa
anthu, ndi kuwafikitsa ku moyo wosatha mwa Yesu Khristu Ambuye athu.

# 6

*Kufa ku Tchimo, Kukhala ndi Moyo mwa Khristu*

1 Nanga tinene chiyani? Kodi tipitirire kuchimwa kuti chisomo
chichulukebe? 2 Ayi. M'njira iliyonse! Popeza tinafa ku tchimo, nanga
tidzapitirira bwanji kukhalabe m'menemo? 3 Kodi simukudziwa kuti tonse
amene tinabatizidwa mwa Khristu Yesu tinabatizidwa mu imfa yake?
4 Chifukwa chake ife tinayikidwa m'manda pamodzi ndi Iye mwa ubatizo.
Tinalowa mu imfa ndi cholinga choti monga momwe Khristu anaukitsidwa
kwa akufa ndi ulemerero wa Atate, ifenso tikakhale m'moyo watsopano.

5 Pakuti ngati ife tinakhala amodzi ndi Iye mu imfa yake, tidzakhalanso
ndithu amodzi ndi Iye mu kuuka kwake. 6 Ife tikudziwa kuti umunthu
wathu wakale unapachikidwa pamodzi ndi Iye kuti thupi la uchimo likhale
lopanda mphamvu ndi kuti tisakakhalenso akapolo a tchimo 7 chifukwa
aliyense amene anafa anamasuka ku tchimo.

8 Koma ngati tinafa pamodzi ndi Khristu, tikhulupirira kuti tidzakha-
lanso ndi moyo pamodzi ndi Iye. 9 Pakuti tikudziwa kuti popeza Khristu
anaukitsidwa kwa akufa, Iye sangafenso. Imfa ilibenso mphamvu pa Iye.
10 Imfa imene Iye anafa, anafa ku tchimo kamodzi kokha, koma moyo
umene akhala ndi wa kwa Mulungu.

11 Kotero inunso, mudzione nokha ngati akufa ku tchimo koma a
moyo kwa Mulungu mwa Khristu Yesu. 12 N'chifukwa chake, musalole
tchimo lilamulire matupi anu amene anafa kuti mumvere zilakolako
zonyansa. 13 Musapereke ziwalo zathupi lanu ku tchimo, ngati zipangizo
zamakhalidwe oyipa. M'malo mwake, mudzipereke kwa Mulungu, ngati
amene achoka ku imfa kupita ku moyo. Ndipo mupereke ziwalo
zathupi lanu ngati zipangizo zachilungamo. 14 Tchimo silidzakhalanso ndi
mphamvu pa inu, chifukwa Malamulo sakulamulira moyo wanu koma
chisomo.

*Ife Ndife Akapolo a Mulungu*

15 N'chiyani tsono? Kodi tidzichimwa chifukwa sitikulamulidwa ndi
Malamulo koma chisomo? Ayi. M'njira iliyonse ayi! 16 Kodi inu
simudziwa kuti pamene mudzipereka kwa wina wake, kumumvera ngati
akapolo, ndinu akapolo a amene mumumvera? Ngati ndinu akapolo
a tchimo mudzafa. Koma ngati ndinu akapolo akumvera, mudzakhala
olungama pamaso pake. 17 Koma ayamikidwe Mulungu pakuti ngakhale
munali akapolo a tchimo, munamvera ndi mtima wonse chiphunzitso
chimene munalandira. 18 Inu munamasulidwa ku tchimo ndipo tsopano
mwasanduka akapolo achilungamo.

19 Ine ndikufanizira zinthu za tsiku ndi tsiku chifukwa chikhalidwe
chanu n'chofowoka. Monga momwe munkapereka ziwalo za matupi
kukhala akapolo a zonyansa ndi makhalidwe oyipa, zimene zimanka
zichulukirabe, choncho tsopano dziperekeni ziwalozo kuti zikhale akapolo
achilungamo ndi a kuyera mtima. 20 Pomwe munali akapolo atchimo,
simunkalabadira za chilungamo. 21 Kodi munapeza phindu lanji pochita
zinthu zimenezi, zomwe tsopano mukuchita nazo manyazi? Zinthu
zimenezo zotsatira zake ndi imfa! 22 Koma tsopano pakuti inu mwa-
masulidwa ku tchimo ndipo mwasanduka akapolo a Mulungu, phindu
lomwe mulipeza ndi kuyera mtima ndipo chotsatira chake ndi moyo
wosatha. 23 Pakuti malipiro a tchimo ndi imfa, koma mphatso yaulere

imene Mulungu amapereka ndi moyo wosatha mwa Khristu Yesu Ambuye athu.

# 7

### *Chitsanzo cha Banja pa Mphamvu za Malamulo*

[1] Kodi simukudziwa abale kuti Malamulo ali ndi ulamuliro pa munthu
pokhapokha ngati ali ndi moyo? Ine ndikuyankhula kwa anthu amene
akudziwa Malamulo. [2] Mwachitsanzo, Malamulo amati mkazi wokwatiwa
ndi womangidwa ndi lamulo kwa mwamuna wakeyo nthawi yonse
pamene mwamuna wakeyo ali moyo. Koma ngati mwamuna wake
amwalira, mkaziyo ndi womasulidwa ku lamulo la ukwati. [3] Koma ngati
iye akwatiwa ndi mwamuna wina pamene mwamuna wake ali moyo, amatchedwa wachigololo. Koma ngati mwamuna wakeyo amwalira, mkaziyo amasuka ku lamulo ndipo si wachigololo, ngakhale kuti wakwatiwa ndi mwamuna wina.
[4] Chimodzimodzi inunso, abale anga, munafa ku Malamulo kudzera
m'thupi la Khristu, kuti mukwatiwe ndi wina, ndi Iye amene anauka kwa
akufa kuti tibalire Mulungu chipatso. [5] Pakuti pamene tinkalamulidwa
ndi khalidwe lathu lauchimo, zilakolako zauchimo zimene Malamulo anaziwutsa zinkagwira ntchito m'matupi mwathu kotero kuti zinabala
imfa. [6] Koma tsopano tamasulidwa ku Malamulowo pakuti tinafa ku
zimene zinkatimanga, ndipo Mzimu Woyera akutithandiza kutumikira Mulungu m'njira yatsopano ndipo osati m'njira yakale yolembedwa.

### *Kulimbana ndi Mphamvu za Tchimo*

[7] Nanga ife tinene chiyani? Kodi Malamulo ndi oyipa? Ayi. N'kosatheka!
Kunena zoona, popanda Malamulo, ine sindikanazindikira tchimo. Pakuti sindikanadziwa kuti kusirira ndi tchimo ngati Malamulo sakananena kuti,
"Usasirire." [8] Koma chifukwa cha Malamulo uchimo unapeza mwayi
owutsa m'kati mwanga khalidwe lililonse la kusirira. Pakuti pakanapanda Malamulo, uchimo ukanakhala wopanda mphamvu. [9] Nthawi
ina ndinali ndi moyo popanda Malamulo. Koma nditayamba kudziwa
Malamulo, pomwepo uchimo unayamba kuphuka, [10] ndipo ine ndinafa.
Ine ndinazindikira kuti Malamulo omwe ankayenera kubweretsa moyo anabweretsa imfa.
[11] Pakuti uchimo unapeza mwayi chifukwa cha Malamulo ndipo kudzera
m'Malamulowo, unandinyenga ndi kundiyika mu imfa. [12] Choncho lamulo
ndi loyera, lolungama ndi labwino. [13] Kodi chomwe ndi chabwino
tsopano chinasanduka imfa kwa ine? Si choncho ayi! Koma kuti uchimo uzindikirike kuti ndi uchimo unabala imfa mwa ine kudzera mu chomwe chinali chabwino, kotero kuti kudzera mu lamulo uchimo ukhale oyipa kopitirira.
[14] Ife tikudziwa kuti Malamulo ndi auzimu; koma ine ndine munthu
wofowoka chabe, wogulitsidwa ngati kapolo ku uchimo. [15] Ine sindizindikira zimene ndimachita. Pakuti zimene ndimafuna kuchita sindizichita koma zimene ndimadana nazo ndi zimene ndimazichita.
[16] Ndipo ngati ndimachita zimene sindimafuna kuzichita, ndiye kuti
ndikuvomereza kuti lamulo ndi labwino. [17] Monga mmene zililimu,
si inenso mwini amene ndimazichita zimenezi, koma tchimo limene
lili m'kati mwanga. [18] Ine ndikudziwa kuti mwa ine mulibe kanthu
kabwino, ndiye kuti m'thupi langa lauchimo. Pakuti ndimafuna kuchita
zabwino, koma ndimalephera kuzichita. [19] Ine sindichita zabwino zimene

ndimafuna koma ndimachita zonyansa zimene sindikuzifuna. [20] Tsopano
ngati ine ndimachita zimene sindikuzifuna, si inenso amene ndimazichita,
koma ndi tchimo limene lili m'kati mwanga.

[21] Tsono ndapeza kuti lamuloli likugwira ntchito. Ngakhale ndima-
funa kuchita zabwino, zoyipa zili nane pomwepo. [22] Mtima wanga
umakondwera ndi lamulo la Mulungu. [23] Koma m'kati mwanga ndimaona
lamulo lina likugwira ntchito kulimbana ndi zomwe mtima wanga
umavomereza. Lamulo limenelo landisandutsa wam'ndende walamulo
la uchimo lomwe likugwira ntchito m'kati mwa ziwalo zanga. [24] Kalanga
ine! Adzandipulumutsa ndani ku thupi la imfali? [25] Atamandike Mulungu,
amene amandipulumutsa kudzera mwa Yesu Khristu Ambuye athu!

Kotero tsono, ineyo ndi mtima wanga ndimatumikira lamulo la Mu-
lungu, koma ndi thupi langa ndimatumikira lamulo la uchimo.

# 8

*Moyo Watsopano mwa Khristu*

[1] Choncho, tsopano amene ali mwa Khristu Yesu alibe mlandu owat-
sutsa [2] chifukwa mwa Khristu Yesu, lamulo la Mzimu Woyera amene
amapereka moyo, lawamasula ku lamulo la tchimo ndi la imfa. [3] Pakuti
zimene Malamulo sanathe kuzichita, popeza anali ofowoka chifukwa
cha khalidwe lathu la uchimo, Mulungu anazichita potumiza Mwana
wake m'chifanizo cha munthu ochimwa kuti akhale nsembe yauchimo.
Ndipo Iye anagonjetsa tchimo m'thupi la munthu, [4] ndi cholinga chakuti
chilungamo chofunikira cha lamulo chikwaniritsidwe kwathunthu mwa
ife amene sitikhala monga mwachikhalidwe chathu cha uchimo koma
mwa Mzimu.

[5] Pakuti anthu amene amakhala monga mwa makhalidwe oyipa a thupi
amayika malingaliro awo pa zinthu zathupi. Koma amene amakhala
monga mwa Mzimu amayika malingaliro awo pa zinthu za Mzimu.
[6] Kuyika mtima pa zathupi ndi imfa koma kuyika mtima pa za Mzimu ndi
moyo ndi mtendere. [7] Pakuti mtima umene wakhazikika pa zathupi ndi
wodana ndi Mulungu. Sunagonjere lamulo la Mulungu ndipo sungathe
kutero. [8] Ndipo anthu amene amalamulidwa ndi khalidwe lauchimo
sangathe kukondweretsa Mulungu.

[9] Koma inu simulamulidwanso ndi khalidwe lanu lauchimo koma ndi
Mzimu ngati Mzimu wa Mulungu akhaladi mwa inu. Koma ngati munthu
aliyense alibe Mzimu wa Khristu, iyeyu si wa Khristu. [10] Ndipo ngati
Khristu ali mwa inu, thupi lanu ndi lakufa chifukwa cha uchimo, koma
mzimu wanu ndi wamoyo chifukwa cha chilungamo. [11] Ndipo ngati
Mzimu wa Mulungu amene anaukitsa Yesu kwa akufa akhala mwa inu,
Iyeyo amene anaukitsa Khristu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu
amene amafa kudzera mwa Mzimu wake amene amakhala mwa inu.

[12] Kotero abale, ife tili ndi zoti tikwaniritse, koma osati za khalidwe
lathu lauchimo, kumachita zofuna zake. [13] Pakuti ngati inu mukhala
monga mwa khalidwe lauchimo, mudzafa. Koma ngati mwa Mzimu
mupha ntchito zoyipa zathupi, mudzakhala ndi moyo. [14] Onse amene
amatsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu ndi ana a Mulungu. [15] Mzimu
amene inu munalandira samakusandutsani akapolo, kuti muzikhalanso
amantha, koma Mzimu amakusandutsani ana. Ndipo mwa Iye ife
timafuwula kuti, "Abba, Atate." [16] Mzimu mwini amavomerezana ndi

mzimu wathu kuti ife ndife ana a Mulungu. 17 Tsono ngati tili ana ake,
ndiye kuti ndife olowa m'malo a Mulungu ndi olowa m'malo pamodzi ndi
Khristu. Ngati ife timva zowawa pamodzi ndi Khristu, tidzalandiranso ndi
ulemerero womwe pamodzi naye.

### *Ulemerero wa M'tsogolo*

18 Ine ndiganiza kuti masautso amene tikuwamva nthawi ino, sak-
ufanana ndi ulemerero umene udzaonetsedwa mwa ife. 19 Pakuti
chilengedwe chikudikira ndi chiyembekezo kuonetsedwa poyera kwa ana
a Mulungu. 20 Pakuti chilengedwe sichinasankhe kugonjera zopanda pake,
koma mwachifuniro cha Iye amene analola kuti chigonjere. Koma chili
ndi chiyembekezo 21 chakuti chidzamasulidwa ku ukapolo wa chivundi
ndi kulandiranso ufulu ndi ulemerero wa ana a Mulungu.

22 Ife tikudziwa kuti chilengedwe chonse chakhala chikubuwula ndi
ululu ngati ululu wa nthawi yobereka mwana mpaka tsopano lino. 23 Si
zokhazo ayi, ngakhale ife tomwe, amene tili ndi zipatso zoyamba za
Mzimu, tikubuwulira m'kati mwathu pomwe tikudikira mwachidwi ku-
sankhidwa kwathu ngati ana, kuwomboledwa kwa matupi athu. 24 Pakuti
ife tinapulumutsidwa m'chiyembekezo ichi. Koma chiyembekezo chimene
chimaoneka si chiyembekezo ayi. Kodi ndani amene amayembekezera
chimene ali nacho kale? 25 Koma ngati ife tiyembekeza chimene tikanalibe,
ndiye kuti tikuyembekeza modekha mtima.

26 Momwemonso, Mzimu amatithandiza ife m'kufowoka kwathu. Ife
sitidziwa momwe tiyenera kupempherera koma Mzimu mwini amatipem-
pherera mobuwula ndi mawu osafotokozedwa. 27 Koma Iye amene amas-
anthula mitima yathu amadziwa maganizo a Mzimu, chifukwa Mzimu
amapempherera oyera mtima molingana ndi chifuniro cha Mulungu.

### *Oposa Agonjetsi*

28 Ndipo ife tikudziwa kuti zinthu zonse zimathandizana kuwachi-
tira ubwino amene amakonda Mulungu, amene anayitanidwa monga
mwa cholinga chake. 29 Pakuti amene Mulungu anawadziwiratu,
anawasankhiratunso kuti akonzedwe m'chifanizo cha Mwana wake, kuti
Iye akhale Mwana woyamba kubadwa mwa abale ambiri. 30 Iwo
amene anawasankhiratu, anawayitananso. Amene Iye anawayitana
anawalungamitsanso ndipo amene anawalungamitsa anawapatsanso ule-
merero.

31 Nanga tsono tidzanena chiyani pa izi? Ngati Mulungu ali mbali yathu,
adzatitsutsa ife ndani? 32 Iye amene sanatimane Mwana wake wa Iye
yekha, koma anamupereka chifukwa cha ife tonse. Iye adzalekeranjinso
pamodzi naye kutipatsa ife zinthu zonse mwaulere? 33 Ndani amene
adzabweretsa mlandu kutsutsa amene Mulungu anawasankha? Ndi
Mulungu amene amalungamitsa. 34 Ndani amene angatipeze ife olakwa?
Palibe. Khristu Yesu amene anafa, kuposera pamenepo, amene anaukit-
sidwa ndi moyo, amene ali kudzanja lamanja la Mulungu ndiye amene
akutipempherera. 35 Ndani amene adzatilekanitsa ife ndi chikondi cha
Khristu? Kodi ndi masautso, kapena zowawa, kapena mazunzo, kapena
njala, kapena umaliseche, kapena choopsa, kapena lupanga? 36 Monga
kwalembedwa:

"Chifukwa cha inu, ife tikuphedwa tsiku lonse:
ife tikutengedwa ngati nkhosa zoti zikaphedwe."

[37] Ayi, mu zonsezi ife ndife oposa agonjetsi mwa Iye amene anatikonda.
[38] Pakuti ine ndatsimikiza ndi mtima wonse kuti ngakhale imfa, kapena
moyo, ngakhale angelo, kapena ziwanda, ngakhale zinthu zilipo, kapena
zili m'tsogolo, kapena mphamvu zina, [39] ngakhale kutalika, kapena kuya,
kapena chilichonse m'chilengedwe chonse, sizingathe kutisiyanitsa ndi
chikondi cha Mulungu chimene chili mwa Khristu Yesu Ambuye athu.

# 9

*Chisankho Chopambana cha Mulungu*

[1] Ine ndikunena zoona mwa Khristu. Sindikunama ndipo chikumbum-
tima changa kudzera mwa Mzimu Woyera chikundichitira umboni. [2] Ndili
ndi chisoni chachikulu ndipo ndikumva kupwetekeka kosalekeza mu
mtima mwanga. [3] Pakuti ndikanafuna ine mwini nditatembereredwa ndi
kuchotsedwa mwa Khristu chifukwa cha abale anga, amene ndi a mtundu
wanga, [4] anthu Aisraeli. Iwo anasankhidwa kukhala ana. Mulungu
anawapatsa ulemerero, anachita nawo mapangano, kuwapatsa Malamulo,
Nyumba yopembedzeramo ndi malonjezano ake. [5] Awo ndi makolo athu.
Kuchokera kwa iwo m'thupi ndi kumene kunachokera makolo a Khristu
Yesu amene ndi Mulungu wolamulira zinthu zonse, alemekezeke mpaka
muyaya! Ameni.

[6] Sikuti mawu a Mulungu analephera. Pakuti si onse obadwa mwa
Israeli amene ndi Israeli. [7] Kapena kuti ana ake chifukwa anachokera mwa
Abrahamu. Koma zidzukulu zako zidzachokera mwa Isake. [8] Kutanthauza
kuti, si ana obadwa m'thupi amene ndi ana a Mulungu koma ndi
ana a lonjezano amene amatengedwa kukhala zidzukulu za Abrahamu.
[9] Pakuti Mulungu analonjeza ponena kuti, "Pa nthawi yake ngati yomwe
ino chaka chamawa ndidzabweranso, ndipo Sara adzakhala ndi mwana
wamwamuna."

[10] Ndipo si pokhapo ayi. Ana awiri a Rebeka aja abambo awo anali
mmodzi, kholo lathu Isake. [11] Komabe, ana amapasawa asanabadwe
kapena asanachite chilichonse chabwino kapena choyipa, n'cholinga choti
chifuniro cha Mulungu chosankhiratu munthu aliyense chipitirire, [12] osati
chifukwa cha ntchito za munthu koma chifuniro cha Iye mwini, anawuza
Rebeka kuti, "Wamkulu adzatumikira wam'ng'ono." [13] Monga momwe
kwalembedwa kuti, "Ine ndinakonda Yakobo, koma ndinamuda Esau."

[14] Nanga tsono tidzanena chiyani? Kodi Mulungu ndi osalungama? Ayi,
ndi pang'ono pomwe! [15] Pakuti Mulungu anawuza Mose kuti,

"Ine ndidzachitira chifundo amene ndikufuna kumuchitira chifundo,
ndipo ndidzakomera mtima amene ndikufuna kumukomera mtima."

[16] N'chifukwa chake, izi sizitengera zokhumba za munthu kapena
kuyesetsa koma chifundo cha Mulungu. [17] Malemba akuti Mulungu
anamuwuza Farao kuti, "Ine ndakuyika kukhala mfumu ndi cholinga choti
ndionetse mphamvu zanga, kuti mwa iwe dzina langa litchuke pa dziko
lonse lapansi." [18] Choncho Mulungu amachitira chifundo munthu amene
akufuna kumuchitira chifundo ndipo amawumitsa mtima munthu amene
Iye akufuna kumuwumitsa mtima.

[19] Tsono mmodzi wa inu n'kundifunsa kuti, "Nanga n'chifukwa chiyani
Mulungu amatipeza olakwa? Nanga ndani amene amakana chifuniro
chake?" [20] Koma ndiwe yani, munthu wamba, woti n'kutsutsana ndi Mu-
lungu? "Kodi chimene chinawumbidwa n'kufunsa amene anachiwumba

kuti, ‘Kodi unandiwumbiranji motere?’ ” 21 Kodi wowumba alibe ufulu
wowumba kuchokera ku dothi lomwelo mbiya yamtengowapatali ndi ina
yamtengo wotsika?
22 Koma Mulungu, anafuna kuonetsa mkwiyo wake ndi kuti mphamvu
yake idziwike. Iye anapirira modekha mtima kwambiri zochita za
anthu omwe anawakwiyirawo amene anayeneradi chiwonongeko. 23 Iye
anachita izi kufuna kuonetsa kulemera kwa ulemerero wake ndi kuti
udziwike kwa amene analandira chifundo chake. Iye anawakonzeratu
kuti alandire ulemerero wake 24 ngakhale ifenso amene anatiyitana osati
kuchokera kwa Ayuda okha komanso kwa a mitundu ina. 25 Monga
momwe Mulungu akunenera m’buku la Hoseya kuti,
“Amene sanali anthu anga ndidzawatcha ‘anthu anga;’
ndipo Ine ndidzatcha ‘wokondedwa wanga’ amene sali wokondedwa wanga,”
26 ndipo,
“Pamalo omwewo pamene ananena kuti,
‘Sindinu anthu anga,’
pomweponso adzawatchula kuti, ‘Ana a Mulungu wamoyo.’ ”
27 Yesaya anafuwula za Aisraeli kuti,
“Ngakhale chiwerengero cha Aisraeli chingakhale ngati mchenga wa ku nyanja,
otsala okha ndiye adzapulumuke.
28 Pakuti Ambuye adzagamula milandu
ya anthu pa dziko lapansi mofulumira ndi kumaliziratu.”
29 Monga momwe Yesaya ananena malo ena kuti,
“Ngati Yehova Wamphamvuzonse
akanapanda kutisiyira zidzukulu,
ife tikanawononongeka
ngati anthu a ku Sodomu, tikanakhala ngati anthu a ku Gomora.”

### *Kusakhulupirira kwa Aisraeli*

30 Kodi nanga tidzati chiyani? Tidzati a mitundu ina amene sanafune
chilungamo analandira chilungamo chachikhulupiriro 31 koma Aisraeli,
amene anafuna chilungamo cha lamulo sanachilandire. 32 Chifukwa
chiyani? Chifukwa iwo sanachifune ndi chikhulupiriro koma ngati mwa
ntchito. Iwo anapunthwa pa “Mwala wopunthwitsa.” 33 Monga momwe
kwalembedwa kuti,
“Taonani, Ine ndikuyika mwala mu Ziyoni wopunthwitsa anthu,
thanthwe limene limagwetsa anthu.
Koma amene akhulupirira Iye sadzachititsidwa manyazi.”

## 10

1 Abale, chokhumba cha mtima wanga ndi pemphero langa kwa Mu-
lungu ndi chakuti Aisraeli apulumutsidwe. 2 Popeza ndiwachitira umboni
kuti ndi achangu pa zinthu za Mulungu koma osati mwachidziwitso.
3 Pakuti sanadziwe chilungamo chochokera kwa Mulungu ndipo anafuna
kukhazikitsa chawochawo. Iwo sanagonjere chilungamo cha Mulungu.
4 Khristu ndiye mathero amalamulo kuti aliyense amene akhulupirira
akhale olungama pamaso pa Mulungu.
5 Mose akulemba motere zachilungamo cha malamulo, “Munthu amene
achita zinthu izi adzakhala ndi moyo pozichita.” 6 Koma chilungamo
cha chikhulupiriro chikuti, “Usanene mu mtima mwako kuti, ‘Kodi ndani

amene akwere kumwamba?' " (ndiko, kukatsitsa Khristu) 7 "kapena 'Ndani
adzatsikira ku dziko la anthu akufa?' " (ndiko, kukamutenga Khristu
kwa akufa). 8 Nanga akuti chiyani? "Mawu ali pafupi ndi inu. Ali
m'kamwa mwanu ndi mu mtima mwanu." Ndiwo mawu achikhulupiriro
amene ife tikuwalalikira, 9 kuti ngati udzavomereza ndi pakamwa pako
kuti, "Yesu ndiye Ambuye," ndi kukhulupirira mu mtima mwako kuti
Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka. 10 Pakuti ndi mtima
wanu mukhulupirira ndi kulungamitsidwa, ndipo ndi pakamwa panu
muvomereza ndi kupulumutsidwa. 11 Pakuti Malemba akuti, "Aliyense
amene akhulupirira Iye, sadzachititsidwa manyazi." 12 Pakuti palibe
kusiyana pakati pa Myuda ndi a mitundu ina, pakuti Ambuye mmodzi
yemweyo ndi Ambuye wa onse ndipo amadalitsa mochuluka onse amene
ayitana pa Iye 13 pakuti, "Aliyense amene adzayitana pa dzina la Ambuye
adzapulumuka."

14 Kodi adzayitana bwanji amene sanamukhulupirire? Ndipo adza-
khulupirira bwanji asanamve za Iye? Ndipo adzamva bwanji popanda
wina kulalikira kwa iwo? 15 Ndipo iwo adzalalikira bwanji osatumidwa?
Kwalembedwa kuti, "Akongoladi mapazi a iwo amene amabweretsa
Uthenga Wabwino!"

16 Koma si onse amene anavomereza Uthenga Wabwino. Pakuti
Yesaya akuti, "Ambuye, ndani amene wakhulupirira uthenga wathu?"
17 Motero, chikhulupiriro chimabwera pamene timva uthenga ndipo
uthenga umamveka kuchokera ku mawu a Khristu. 18 Koma ndikufunsa
kuti kodi iwo anamva? Inde, iwo anamva kuti,

"Liwu lawo linamveka ponseponse pa dziko lapansi.
Mawu awo anafika ku malekezero a dziko lonse."

19 Ine ndifunsanso kuti, kodi Israeli sanazindikire? Poyamba Mose akuti,

"Ine ndidzawachititsa kuti achite nsanje ndi mtundu wina wopandapake.
Ine ndidzawakwiyitsa ndi mtundu wina wachabechabe."

20 Ndipo Yesaya molimba mtima akuti,

"Anandipeza anthu amene sanali kundifunafuna.
Ndinadzionetsera kwa amene sanafunse za Ine."

21 Koma zokhudzana ndi Aisraeli akuti,

"Tsiku lonse ndinatambasulira manja anga
kwa anthu osandimvera ndi okanika."

# 11

*Aisraeli Otsala*

1 Ine ndikufunsa kuti kodi Mulungu anakana anthu ake? Ayi. Ndi
pang'ono pomwe! Inenso ndine Mwisraeli, mmodzi mwa zidzukulu za
Abrahamu, ndiponso wa fuko la Benjamini. 2 Mulungu sanawakane anthu
ake amene Iye anawadziwiratu. Kodi inu simukudziwa zimene Malemba
akunena pa ndime imene Eliya akudandaula kwa Mulungu kuneneza
Aisraeli? Iye anati, 3 "Ambuye, anthuwa apha aneneri anu ndi kugwetsa
maguwa anu ansembe. Ndatsala ine ndekha wamoyo ndipo akufuna
kundipha?" 4 Ndipo yankho la Mulungu linali lotani? "Ine ndadzisungira
ndekha anthu 7,000 amene sanapembedzepo Baala." 5 Chimodzimodzinso
lero lino, alipo Aisraeli pang'ono osankhidwa mwachisomo. 6 Ndipo
ngati ndi mwachisomo, sikungakhalenso mwa ntchito. Ngati zikanatero,
chisomo sichikanakhalanso chisomo ayi.

[7] N'chiyani tsopano? Chimene Aisraeli anachifuna ndi mtima wonse
sanachipeze koma osankhidwawo anachipeza. Enawo anawumitsidwa
mtima [8] monga kwalembedwa kuti,
"Mulungu anawapatsa mzimu wosatha kumvetsa zinthu,
maso osatha kupenya;
makutu osatha kumva
mpaka lero lino."
[9] Ndipo Davide akuti,
"Maphwando awo asanduke msampha ndi diwa lowakola
ndi chopunthwitsa kuti alandire chilango.
[10] Maso awo atsekedwe kuti asaone,
ndi misana yawo ikhale yokhota nthawi zonse."

### *Nthambi Zomangiririridwa*

[11] Ine ndikufunsanso kuti, kodi iwo anapunthwa ndi kugwa kotheratu?
Ayi. Ndi pang'ono pomwe! Koma chifukwa cha kulakwa kwawo, chipu-
lumutso chinafika kwa a mitundu ina kuti Aisraeli achite nsanje. [12] Koma
ngati kulakwa kwawo kwapindulitsa dziko lapansi ndi kulephera kwawo
kwapindulitsa a mitundu ina, nanga kudzakhala kupindula kwakukulu
chotani iwo akadzabwera chonse!
[13] Ine ndikuyankhula kwa inu a mitundu ina monga ine ndili mtumwi
wa kwa a mitundu ina ndipo ndimawunyadira utumiki wangawu. [14] Ine
cholinga changa n'chakuti ndichititse nsanje anthu a mtundu wanga
kuti ena mwa iwo apulumutsidwe. [15] Pakuti ngati kukanidwa kwawo
kunayanjanitsa anthu a dziko lapansi ndi Mulungu, nanga kudzatani,
Iye akadzawalandiranso? Kudzakhala monga ngati anthu akufa akuuka.
[16] Ngati chigawo chimodzi cha buledi woperekedwa monga zipatso
zoyamba ndi choyera, ndiye kuti zonsezo ndi zoyera. Ngati muzu ndi
oyera, n'chimodzimodzinso nthambi zake.
[17] Ngati nthambi zina zinakhadzulidwa ndipo inu, inu ndiye nthambi
za olivi wakuthengo, n'kulumikizidwa pamalo pa nthambi zimenezo,
ndipo tsopano mukulandira nawo zakudya zochokera ku mizu ya olivi,
[18] musadzitame kunyoza nthambi zinazo. Ngati mutero, ganizirani ichi
kuti Inu simugwiriziza mizu, koma muzu ukugwiriziza inu. [19] Tsono
mudzati, "Nthambizo zinakhadzulidwa kuti ine ndilumikizidwepo."
[20] N'zoona. Koma iwo anakhadzulidwa chifukwa chosakhulupirira ndipo
inu mukuyima mwachikhulupiriro. Musadzitukumule, koma muchite
mantha. [21] Pakuti ngati Mulungu sanalekerere nthambi zachibadwidwe,
Iye sadzakulekererani inunso.
[22] N'chifukwa chake ganizirani za kukoma mtima ndi za ukali wa
Mulungu. Ukali uli kwa iwo amene anagwa koma kukoma mtima kwa
inu, malinga ngati musamala kukoma mtima kwakeko kupanda kutero
inunso mudzakhadzulidwanso. [23] Ngati iwo asiya kukhala osakhulupirira,
adzalumikizidwanso pakuti Mulungu akhoza kuwalumikizanso. [24] Pakuti
ngati inu, mwa chilengedwe munali mtengo wa olivi wa kuthengo, Mu-
lungu anakukhadzulani nakulumikizani ku mtengo wa olivi wodzalidwa,
zomwe ndi zotsutsana ndi chilengedwe, kodi sikudzakhala kwapafupi kwa
Iye kuwalumikizanso mu mtengo wawowawo wa olivi?

### *Aisraeli Onse Adzapulumuka*

[25] Abale, ine sindifuna kuti mukhale osadziwa za chinsinsi ichi, kuti
mungadziyese nokha anzeru. Kuwuma mtima kumene Aisraeli akuchita

ndi kwa kanthawi kufikira chiwerengero cha a mitundu chitalowa.
26 Kotero tsono Aisraeli onse adzapulumuka, monga kwalembedwa kuti,
"Mpulumutsi adzachokera ku Ziyoni;
Iye adzachotsa zoyipa zonse za Yakobo.
27 Ndipo ili lidzakhala pangano langa ndi iwo
pamene Ine ndidzachotsa machimo awo."
28 Chifukwa cha Uthenga Wabwino, Aisraeli asanduka adani a Mulungu
kuti inu mupindule. Koma kunena za kusankhidwa, iwo ndi okondedwa
ndi Mulungu chifukwa cha makolo awo aja. 29 Pakuti Mulungu akayitana
munthu ndi kumupatsa mphatso sangasinthenso. 30 Monga mmene
inu munalili, osamvera Mulungu pa nthawi ina, tsopano mwalandira
chifundo chifukwa cha kusamvera kwawo. 31 Chonchonso iwo akhala
osamvera tsopano kuti iwonso alandire chifundo chifukwa cha chifundo
cha Mulungu kwa inu. 32 Pakuti Mulungu anasandutsa anthu onse a
m'ndende ya kusamvera kuti Iye akaonetse chifundo kwa onse.

### *Kulemekeza Mulungu*

33 Aa! Nzeru za Mulungu ndi chidziwitso chake ndi zozama kwambiri!
Ndani angazindikire maweruzidwe ake,
ndipo njira zake angazitulukire ndani?
34 "Kodi wadziwa ndani maganizo a Ambuye?
Kapena ndani anakhalapo mlangizi wake?"
35 "Kodi ndani anapereka mphatso kwa Mulungu,
kuti Mulunguyo amubwezere iye?"
36 Pakuti zinthu zonse n'zochokera kwa Iye, n'zolengedwa ndi Iye ndipo
zimabweretsa ulemerero kwa Iye.
Kwa Iye kukhale ulemerero mpaka muyaya! Ameni.

## 12

### *Nsembe za Moyo*

1 N'chifukwa chake ine ndikukupemphani abale, mwa chifundo cha
Mulungu, kuti mupereke matupi anu monga nsembe yamoyo, yopatulika
ndi yokondweretsa Mulungu. Nsembeyi ndiye kupembedza kwanu kwa
uzimu. 2 Musafanizidwenso ndi makhalidwe a dziko lino koma musan-
dulike pokonzanso maganizo anu. Ndipo mudzadziwa ndi kuzindikira
chifuniro chabwino cha Mulungu chomwe ndi chokondweretsa ndi
changwiro.
3 Chifukwa cha chisomo chopatsidwa kwa ine, ndinena kwa aliyense
wa inu kuti musadziyenereze nokha kuposa mmene mulili. Koma mudzi-
ganizire nokha modzichepetsa, molingana ndi muyeso wa chikhulupiriro
chimene Mulungu wakupatsani. 4 Pakuti monga aliyense wa ife ali ndi
thupi limodzi koma ziwalo zambiri, ziwalozi sizili ndi ntchito yofanana.
5 Momwemonso mwa Khristu ife amene tili ambiri tipanga thupi limodzi
ndipo chiwalo chilichonse ndi cholumikizika ku chinzake. 6 Ife tili
ndi mphatso zosiyana, molingana ndi chisomo chopatsidwa kwa ife.
Ngati mphatso ya munthu ndi kunenera, musiyeni ayigwiritse ntchito
molingana ndi chikhulupiriro chake. 7 Ngati ndi kutumikira, musiyeni
atumikire. Ngati ndi kuphunzitsa, musiyeni aphunzitse. 8 Ngati ndi
kulimbikitsa, musiyeni alimbikitse. Ngati ndi kupereka kuthandiza osowa,
musiyeni apereke mowolowamanja. Ngati ndi utsogoleri, musiyeni

alamulire mosamala. Ngati ndi kuonetsa chifundo, musiyeni achite mosangalala.

*Chikondi*

9 Chikondi chikhale chopanda chinyengo. Dana nacho choyipa;
gwiritsitsa chabwino. 10 Mukondane kwathunthu monga abale.
Lemekezanani wina ndi mnzake kuposa inu eni. 11 Musakhale aulesi
m'machitidwe anu. Khalani achangu mu mzimu ndipo tumikirani
Ambuye. 12 Kondwerani m'chiyembekezo, piririni m'masautso ndiponso
khulupirikani m'pemphero. 13 Gawananani ndi anthu a Mulungu amene ali
ndi chosowa. Cherezani alendo.
14 Adalitseni amene akuzunzani. Adalitseni ndipo musawatemberere.
15 Kondwani pamodzi ndi amene akukondwa ndipo lirani ndi amene
akulira. 16 Muyanjane wina ndi mnzake. Musakhale onyada, koma lolani
kuyanjana ndi anthu wamba. Musaganize kuti mumadziwa zonse.
17 Musabwezere choyipa ndi choyipa kwa aliyense. Samalitsani kuchita
chabwino pamaso pa aliyense. 18 Ngati n'kotheka, khalani mwamten-
dere ndi aliyense monga momwe mungathere. 19 Okondedwa anga,
musabwezere choyipa, koma lekerani Mulungu. Pakuti kwalembedwa,
"Kubwezera chilango n'kwanga. Ndidzawalanga ndine," akutero Ambuye.
20 Koma,

"Ngati mdani wako ali ndi njala, mupatse chakudya.
Ngati ali ndi ludzu, mupatse kanthu kakumwa.
Pochita ichi, udzamuwunjikira makala amoto pamutu pake."

21 Musagonjetsedwe ndi choyipa, koma gonjetsani choyipa pochita chab-
wino.

# 13

*Kumvera Aulamuliro*

1 Aliyense ayenera kumvera akulu olamulira, chifukwa palibe ulamuliro
umene sunachokere kwa Mulungu. Olamulira amene alipo anayikidwa
ndi Mulungu. 2 Kotero kuti, iwo amene awukira ulamuliro atsutsana
ndi chimene Mulungu anakhazikitsa. Ndipo amene atero adzibweretsera
okha chilango. 3 Pakuti olamulira saopseza amene amachita zabwino
koma amene amachita zoyipa. Kodi mukufuna kukhala osaopa olamulira?
Tsono chitani zoyenera ndipo adzakuyamikirani. 4 Pakuti iyeyo ndi
mtumiki wa Mulungu wokuchitirani zabwino. Koma ngati muchita
zoyipa muchite mantha, pakuti iye ali ndi mphamvu zolangira. Iye ndi
mtumiki wa Mulungu wobweretsa mkwiyo ndi kulanga onse ochita zoyipa.
5 N'chifukwa chake ndi koyenera kugonjera olamulira, osati chifukwa
choopa kulangidwa kokha komanso chifukwa cha chikumbumtima. 6 Ichi
n'chifukwa chakenso inu mumapereka msonkho. Pakuti olamulira ndi
atumiki a Mulungu amene amapereka nthawi yawo yonse kulamulira.
7 Mubwezereni aliyense amene munamukongola. Ngati inu muli ndi
ngongole yamsonkho, perekani msonkho kwa oyenera kuwalipira. Ngati
ndi kuopa perekeni kwa oyenera kuwaopa ndipo ngati ndi ulemu kwa
oyenera ulemu.

*Chikondi Chimakwaniritsa Malamulo*

8 Musakhale ndi ngongole ndi wina aliyense kupatula ngongole ya
kukondana wina ndi mnzake. Pakuti amene amakonda munthu mnzake
wakwaniritsa lamulo. 9 Malamulo awa: "Usachite chigololo," "Usaphe,"

“Usabe,” “Usasirire,” ndi malamulo ena onse amene alipo, akhazikika pa
lamulo limodzi ili, “Konda mnansi wako monga iwe mwini.” 10 Chikondi
sichichitira mnzake zoyipa. Chifukwa chake chikondi ndicho chokwanir-
itsa lamulo.
11 Ndipo chitani ichi pozindikira nthawi ino. Nthawi yafika yoti inu
mudzuke kutulo, chifukwa chipulumutso chathu chili pafupi tsopano
kuposa pamene tinayamba kukhulupirira. 12 Usiku watsala pafupifupi
kutha. Kwatsala pang’ono kucha. Tiyeni tsono tichotse ntchito zamdima
ndipo tivale chovala chakuwunika. 13 Tiyeni tikhale moyenera monga
nthawi ya masana, osati m’magulu amadyerero, achiwerewere ndi
kuledzera, m’madama ndi zonyansa komanso osati m’magawano ndi
nsanje. 14 Koma valani Ambuye Yesu Khristu ndipo musaganizire za
momwe mungakwaniritsire zokhumba zachikhalidwe cha uchimo.

# 14

*Ofowoka ndi Amphamvu*

1 Mulandire amene ndi ofowoka m’chikhulupiriro, osatsutsana naye
pa maganizo ake. 2 Chikhulupiriro cha munthu wina chimamulola
kudya china chilichonse koma munthu wina, amene chikhulupiriro
chake ndi chofowoka, amangodya zamasamba zokha. 3 Munthu amene
amadya chilichonse sayenera kunyoza amene satero, ndipo munthu
amene samadya chilichonse asaweruze munthu amene amatero, pakuti
Mulungu anamulandira. 4 Kodi ndiwe ndani kuti uweruze wantchito
wamwini? Mbuye wake yekha ndiye aweruze ngati iye wakhoza kapena
walephera pa ntchito yake. Ndipo adzakhoza popeza kuti Mbuye wake
angathe kumukhozetsa.
5 Munthu wina amayesa tsiku limodzi lopatulika kuposa lina. Munthu
wina amayesa masiku onse ofanana. Aliyense akhale otsimikiza
m’maganizo ake. 6 Iye amene amaganiza kuti tsiku limodzi ndi lopam-
bana, amatero kwa Ambuye. Iye amene amadya nyama, amadya mwa
Ambuye pakuti amayamika Mulungu. Ndipo iye amene sadya, amatero
kwa Ambuye ndi kuyamika Mulungu. 7 Pakuti palibe wina wa ife amene
amakhala moyo pa yekha ndiponso palibe wina wa ife amene amafa pa
yekha. 8 Ngati ife tikhala ndi moyo, ife tikhala ndi moyo kwa Ambuye.
Ndipo ngati ife tifa, tifa kwa Ambuye. Choncho, ngati tikhala ndi moyo
kapena kufa, ndife ake a Ambuye.
9 Pa chifukwa ichi, Khristu anafa ndi kuukanso kotero kuti Iye akhale
ndi Ambuye wa akufa ndi amoyo. 10 Tsono n’chifukwa chiyani iwe
ukuweruza m’bale wako? Kapena n’chifukwa chiyani ukumunyoza
m’bale wako? Pakuti ife tonse tidzayima pa mpando wakuweruza wa
Mulungu. 11 Kwalembedwa, akutero Ambuye,
“Pamene Ine ndili ndi moyo,
aliyense adzandigwadira
ndipo lilime lililonse lidzavomereza Mulungu.”
12 Choncho tsopano, aliyense wa ife adzafotokoza yekha kwa Mulungu.
13 Motero, tiyeni tisiye kuweruzana wina ndi mnzake. M’malo mwake,
tsimikizani m’maganizo anu kuti musayike chokhumudwitsa kapena
chotchinga m’njira ya m’bale wanu. 14 Monga mmodzi amene ndili
mwa Ambuye Yesu, ndine wotsimikiza mtima kuti palibe chakudya
chimene pachokha ndi chodetsedwa. Koma ngati wina atenga china

chake kukhala chodetsedwa, kwa iyeyo ndi chodetsedwa. [15] Ngati
m'bale wako akuvutika chifukwa cha chimene umadya, iwe sukuchitanso
mwachikondi. Usamuwononge m'bale wako amene Khristu anamufera
chifukwa cha chakudya chakocho. [16] Musalole kuti chimene muchiyesa
chabwino achinene ngati choyipa. [17] Pakuti Ufumu wa Mulungu si nkhani
yakudya ndi kumwa, koma chilungamo, mtendere ndi chimwemwe mwa
Mzimu Woyera. [18] N'chifukwa chake aliyense amene atumikira Khristu
m'njira iyi akondweretsa Mulungu ndi kuvomerezedwa ndi anthu.

[19] Tsono tiyeni tiyesetse kuchita zimene zidzabweretsa mtendere ndi
kulimbikitsana mwachikondi. [20] Musawononge ntchito ya Mulungu
chifukwa cha chakudya. Chakudya chonse ndi choyera, koma munthu
amalakwa ngati adya chilichonse chimene chimakhumudwitsa wina.
[21] N'kwabwino kusadya kapena kumwa vinyo kapena kuchita chilichonse
chimene chidzachititsa m'bale wako kugwa.

[22] Tsono zimene ukukhulupirira pa zinthu izi zikhale pakati pa iwe
ndi Mulungu. Wodala munthu amene sadzitsutsa yekha pa zimene
amazivomereza. [23] Koma munthu amene akukayika atsutsidwa ngati
adya, chifukwa kudya kwake si kwa chikhulupiriro; ndipo chilichonse
chosachokera m'chikhulupiriro ndi tchimo.

# 15

[1] Ife amene tili ndi chikhulupiriro champhamvu tiziwalezera mtima
anthu ofowoka, ndipo tisamadzikondweretse tokha. [2] Aliyense wa ife
akondweretse mnzake pomuchitira zabwino zomulimbikitsa. [3] Pakuti
ngakhale Khristu sanadzikondweretsa yekha koma, monga kwalembedwa
kuti, "Chipongwe cha anthu okunyozani chinagwera Ine." [4] Pakuti
zilizonse zimene zinalembedwa kale zinalembedwa kuti zitiphunzitse ife.
Malembawo amatilimbikitsa kupirira kuti tikhale ndi chiyembekezo.

[5] Mulungu amene amapereka kupirira ndi chilimbikitso akupatseni
maganizo amodzi pakati panu monga inu mukutsatira Khristu Yesu,
[6] kotero kuti ndi mtima umodzi ndi movomerezana mulemekeze Mulungu
ndi Atate a Ambuye athu Yesu Khristu.

[7] Tsopano landiranani wina ndi mnzake, monganso Khristu anakulandi-
rani inu, ndi cholinga choti Mulungu alemekezeke. [8] Chifukwa kunena
zoona, Khristu wasanduka mtumiki wa Ayuda, kuonetsa kuti Mulungu
ndi wokhulupirika pa malonjezo amene anachita kwa makolo awo [9] kuti
a mitundu ina atamande Mulungu chifukwa cha chifundo chake. Monga
kwalembedwa kuti,

"Choncho ine ndidzakutamandani pakati pa a mitundu;
ndidzayimba nyimbo zotamanda dzina lanu."

[10] Akutinso,

"Kondwerani inu anthu a mitundu ina pamodzi ndi anthu ake."

[11] Ndipo akutinso,

"Tamandani Ambuye, inu nonse a mitundu ina,
ndi kuyimba zotamanda Iye, inu anthu onse."

[12] Ndiponso Yesaya akuti,

"Muzu wa Yese udzaphuka,
wina amene adzauka kulamulira anthu a mitundu ina;
mwa Iye mudzakhala chiyembekezo cha a mitundu ina."

13 Mulungu amene amatipatsa chiyembekezo adzaze mitima yanu ndi
chimwemwe ndi mtendere pamene mukumudalira Iye, kuti chiyembekezo
chanu chisefukire mwamphamvu ya Mzimu Woyera.

### *Paulo Mtumwi wa Anthu a Mitundu Ina*

14 Abale anga, ine mwini ndikutsimikiza kuti inuyo ndinu abwino,
odzaza ndi chidziwitso ndi okhoza kulangizana wina ndi mnzake.
15 Ine ndakulemberani inu molimba mtima pa fundo zina, kukhala
ngati kukukumbutsaninso za zimenezo, chifukwa cha chisomo chimene
Mulungu anandipatsa ine 16 kukhala mtumiki wa Khristu Yesu wa a
mitundu ina ndi udindo wa wansembe, kulalikira Uthenga Wabwino wa
Mulungu, kuti a mitundu ina akhale nsembe yolandiridwa kwa Mulungu,
yopatsidwa ndi Mzimu Woyera.
17 Choncho, ine ndikunyadira mwa Khristu Yesu potumikira Mulungu
wanga. 18 Ine sindidzayesera kuyankhula za kanthu kalikonse koma
zimene Khristu wazichita kudzera mwa ine zotsogolera a mitundu ina kuti
amvere Mulungu mwa zimene ndinanena ndi kuzichita 19 mwamphamvu
ya zizindikiro ndi zodabwitsa kudzera mwamphamvu ya Mzimu Woyera.
Choncho kuchokera ku Yerusalemu ndi kuzungulira ku Iluriko, ine ndala-
likira kwathunthu Uthenga Wabwino wa Khristu. 20 Chakhala chilakolako
changa nthawi zonse kuti ndilalikire Uthenga Wabwino kumene Khristu
sadziwika, kuti ine ndisamange pa maziko a wina wake. 21 Koma monga
kwalembedwa kuti,
"Iwo amene sanawuzidwe za Iye adzaona,
ndi iwo amene sanamve adzazindikira."
22 Ichi n'chifukwa chake ine ndakhala ndikuletsedwa kawirikawiri kubw-
era kwa inu.

### *Paulo Akonza Zopita ku Roma*

23 Koma tsopano popeza kulibenso malo anga woti ndigwire ntchito
m'madera awa, ndakhala ndikufuna kukuonani kwa zaka zambiri. 24 Ine
ndikukonza kuti nditero pamene ndipita ku Spaniya. Ine ndikuyembekeza
kudzakuchezerani pamene ndikudutsa ndi kuti inu mudzathandize popi-
tiriza ulendo wanga, nditasangalala ndi kukhala nanu kwa kanthawi.
25 Koma tsopano, ine ndili pa ulendo wopita ku Yerusalemu potumikira
oyera mtima akumeneko. 26 Pakuti kunakomera a ku Makedoniya ndi
a ku Akaya kupereka thandizo kwa osauka pakati pa oyera mtima mu
Yerusalemu. 27 Iwo chinawakomera kuchita ichi, ndipo ndithu anali
ndi ngongole kwa iwo. Pakuti ngati a mitundu ina anagawana ndi
Ayuda madalitso auzimu, iwo ali ndi ngongole kwa Ayuda kuti agawane
nawo madalitso awo a ku thupi. 28 Tsono ine nditamaliza ntchito iyi
ndi kutsimikiza kuti alandira chipatsochi, ndidzadzera kwanuko kudza-
kuchezerani pa ulendo wanga popita ku Spaniya. 29 Ine ndikudziwa kuti
pamene ndidzabwera kwa inu, ndidzafika ndili wodzaza ndi madalitso a
Khristu.
30 Abale, ine ndikukupemphani, mwa Ambuye athu Yesu Khristu ndi
mwachikondi cha Mzimu, kuti mukhale nane pa kulimbika kwanga
pondipempherera kwa Mulungu. 31 Pempherani kuti ine ndilanditsidwe
kwa osakhulupirira a ku Yudeya ndi kuti utumiki wanga mu Yerusalemu
ukhale ovomerezeka ndi oyera mtima. 32 Kuti mwachifuniro cha Mulungu
ndibwere kwa inu ndi chimwemwe kuti ndidzapumule pamodzi ndi inu.
33 Mulungu wamtendere akhale ndi inu nonse. Ameni.

# 16

*Mawu Olawirana*

1 Ine ndikupereka kwa inu mlongo wathu Febe, mtumiki wa mpingo wa
ku Kenkreya. 2 Ine ndikukupemphani kuti mumulandire mwa Ambuye
m'njira yoyenera oyera mtima ndi kumupatsa thandizo lililonse limene
akulifuna kuchokera kwa inu, pakuti iye wakhala thandizo lalikulu kwa
anthu ambiri kuphatikiza ine.

3 Perekani moni kwa Prisila ndi Akura, atumiki anzanga mwa Khristu
Yesu. 4 Iwo anapereka miyoyo yawo chifukwa cha ine. Osati ine
ndekha komanso mipingo yonse ya a mitundu ina ikuyamika.
5 Perekaninso moni kwa mpingo umene umasonkhana m'nyumba mwawo.
Perekani moni kwa m'bale wanga wokondedwa Epeneto, amene ndi woyamba kukhulupirira Khristu m'chigawo cha Asiya.
6 Perekani moni kwa Mariya, amene wakhala akukugwirirani ntchito kwambiri.
7 Perekani moni kwa Androniko ndi Yuniya abale anga amene anali m'ndende pamodzi ndi ine. Iwo amadziwika ndi atumwi, ndipo iwo anali mwa Khristu ine ndisanakhale.
8 Perekani moni kwa Ampliato, amene ine ndimamukonda mwa Ambuye.
9 Perekani moni kwa Urbano, mtumiki mnzathu mwa Khristu ndi wokondedwa wanga Staku.
10 Perekani moni kwa Apele, woyesedwa ndi wovomerezeka mwa Khristu.
Perekani moni kwa a m'banja la Aristobulo.
11 Perekani moni kwa Herodiona, m'bale wanga.
Perekani moni kwa a m'banja la Narkiso amene ali mwa Ambuye.
12 Perekani moni kwa Trufena ndi Trufosa, amayi aja amene amagwira ntchito ya Ambuye molimbika.
Perekani moni kwa mnzanga wokondedwa Persida, mayi winanso amene wagwira ntchito kwambiri mwa Ambuye.
13 Perekani moni kwa Rufo, wosankhidwa mwa Ambuye, ndi amayi ake, amene akhala amayi anganso.
14 Perekani moni kwa Asunkrito, Felego, Herima, Patroba, Herima ndi abale amene ali nawo pamodzi.
15 Perekani moni kwa Filologo, Yuliya, Neriya ndi mlongo wake, ndi Olumpa ndi oyera mtima onse amene ali nawo pamodzi.
16 Mupatsane moni wina ndi mnzake mwachikondi choona.
Mipingo yonse ya Khristu ikupereka moni.

17 Abale, ine ndikukupemphani kuti musamale chifukwa cha amene
ayambitsa mipatuko ndi kuyika zokhumudwitsa panjira yanu, motsutsana
ndi chiphunzitso chimene mwachiphunzira. Muwapewe iwo. 18 Pakuti
otero sakutumikira Ambuye athu Khristu koma zilakolako zawo. Ndi
mawu okoma ndi oshashalika iwo amanamiza anthu osalakwa. 19 Aliyense
anamva za kumvera kwanu, choncho ndine odzaza ndi chimwemwe
chifukwa cha inu. Koma ine ndikufuna kuti inu mukhale anzeru pa
zabwino, ndi wopanda cholakwa pa zimene zili zoyipa.

20 Mulungu wamtendere adzaphwanya Satana msanga pansi pa mapazi
anu.

Chisomo cha Ambuye athu Yesu chikhale ndi inu.

21 Timoteyo, mtumiki mnzanga, akupereka moni. Nawonso, Lusio, Yasoni ndi Sosipatro, abale anga akutero.

22 Ine Tertio, amene ndalemba kalatayi, ndi kupereka moni mwa Ambuye.

23 Gayo, amene chifukwa cha chisamaliro chake, ine ndi mpingo wonse kuno tikusangalala, akupereka moni.

Erasto, amene ndi msungichuma wa mzinda wonse ndiponso m'bale wathu Kwato, akupereka moni.

24 Chisomo cha Ambuye athu Yesu Khristu chikhale ndi inu nonse. Ameni.

25 Tsopano kwa Iye amene ali ndi mphamvu yokhazikitsa monga mwa
uthenga wanga wabwino ndikulalikidwa kwa Yesu Khristu, monga mwa
vumbulutso lachinsinsi chobisika kwa nthawi yayitali,
26 koma tsopano
chavumbulutsidwa ndi kudziwika kudzera m'Malemba a uneneri mwa
lamulo la Mulungu wosatha, kuti mitundu yonse ikhulupirire ndi kumvera
Iye,
27 kwa Mulungu yekhayo wanzeru kukhale ulemerero kwamuyaya
kudzera mwa Yesu Khristu! Ameni.

# KALATA YOYAMBA YA PAULO YOLEMBERA AKORINTO

1 Paulo, woyitanidwa mwachifuniro cha Mulungu kuti akhale mtumwi
wa Khristu Yesu ndi m'bale wathu Sositene.
2 Kupita ku mpingo wa Mulungu ku Korinto, kwa oyeretsedwa mwa
Khristu Yesu ndi oyitanidwa kukhala opatulika ndiponso kwa onse amene
amapemphera m'dzina la Ambuye athu Yesu Khristu m'dziko lonse
lapansi, amene ndi Ambuye wawo ndi wathunso.
3 Landirani chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate athu
ndi Ambuye athu Yesu Khristu.

*Kuthokoza*

4 Nthawi zonse ndimayamika Mulungu chifukwa cha inu chifukwa
cha chisomo chake chopatsidwa kwa inu mwa Khristu Yesu. 5 Pakuti
mwa Iye mwalemekezedwa m'njira iliyonse, m'kuyankhula kwanu konse
ndi m'kudziwa kwanu konse, 6 chifukwa umboni wathu pa za Khristu
unatsimikizidwa mwa inu. 7 Choncho inu simusowa mphatso yauzimu
iliyonse pamene mukudikira mofunitsitsa kuti Ambuye athu Yesu Khristu
avumbulutsidwe. 8 Adzakulimbikitsani mpaka kumapeto kuti mudzakhale
wopanda mlandu pa tsiku lobwera Ambuye athu Yesu Khristu. 9 Mulungu
amene wakuyitanani inu mu chiyanjano ndi Mwana wake Yesu Khristu
Ambuye athu ngokhulupirika.

*Kugawikana mu Mpingo*

10 Ndidandaulira inu, abale, m'dzina la Ambuye athu Yesu Khristu kuti
nonsenu muvomerezane wina ndi mnzake kuti pasakhale kugawikana
pakati panu ndi kuti mukhale amodzi kwenikweni mu nzeru ndi
m'maganizo. 11 Abale anga, ena a ku nyumba ya Kloe andidziwitsa
kuti pali mkangano pakati panu. 12 Chimene ndikutanthauza ndi ichi:
wina amati, "Ndimatsatira Paulo," wina, "Ndimatsatira Apolo," wina,
"Ndimatsatira Kefa," winanso, "Ndimatsatira Khristu."
13 Kodi Khristu wagawikana? Kodi Paulo anapachikidwa pa mtanda
chifukwa cha inu? Kodi munabatizidwa m'dzina la Paulo? 14 Ine
ndikuyamika kuti sindinabatizepo mmodzi mwa inu kupatula Krispo ndi
Gayo, 15 mwakuti palibe amene anganene kuti anabatizidwa m'dzina
langa. 16 (Inde, ine ndinabatizanso a m'banja la Stefano, koma
sindikumbukira ngati ndinabatizanso wina aliyense). 17 Pakuti Khristu
sananditume ine kudzabatiza, koma kudzalalikira Uthenga Wabwino,
osati ndi mawu anzeru za umunthu, kuopa kuti mtanda wa Khristu
ungakhale wopanda mphamvu.

*Khristu ndiye Nzeru ndi Mphamvu za Mulungu*

18 Pakuti uthenga wa mtanda ndi chopusa kwa iwo amene aku-
wonongeka, koma kwa ife amene tikupulumutsidwa uthengawu ndi
mphamvu ya Mulungu. 19 Pakuti kwalembedwa kuti,
"Ine ndidzawononga nzeru za anthu anzeru;
luntha la anthu aluntha Ine ndidzalinyoza."
20 Munthu wanzeru ali kuti? Munthu wozama ndi maphunziro ali kuti?
Munthu wodziwa zakuya zamakono ali kuti? Kodi Mulungu sanazipusitse
nzeru za dziko lapansi? 21 Tsono poti mwa nzeru za Mulungu dziko

lapansi mu nzeru zake silinamudziwe Iye, Mulungu amakondweretsedwa
kuti kudzera mu chopusa cha zomwe zinalalikidwa apulumutse iwo
amene akhulupirira. 22 Ayuda amafuna zizindikiro zodabwitsa ndipo
Agriki amafunafuna nzeru, 23 koma ife timalalikira Khristu wopachikidwa.
Chitsa chokhumudwitsa kwa Ayuda ndi chopusa kwa a mitundu ina.
24 Koma kwa iwo amene Mulungu anawayitana, Ayuda ndi Agriki omwe,
Khristu ndi mphamvu ya Mulungu ndi nzeru za Mulungu. 25 Pakuti za
Mulungu zooneka ngati zopusa, ndi za nzeru kuposa nzeru za munthu,
ndipo za Mulungu zooneka ngati zofowoka, zili ndi mphamvu kuposa
mphamvu za munthu.

26 Abale taganizirani mmene munalili musanayitanidwe. Si ambiri a
inu munali a nzeru, si ambiri a inu munali a mphamvu zamakopedwe. Si
ambiri a inu munali obadwa pa ulemerero. 27 Koma Mulungu anasankha
zinthu zopusa za dziko lapansi kuti achititse manyazi anzeru. Mulungu
anasankha zinthu zofowoka za dziko lapansi kuti achititse manyazi
amphamvu. 28 Anasankha zinthu zapansipansi ndi zopeputsidwa za dziko
la pansi lino, zinthu zimene kulibe, kuti asukulutse zimene zilipo, 29 kuti
munthu asanyade pamaso pa Mulungu. 30 N'chifukwa cha Iye kuti inu
muli mwa Khristu Yesu, amene wakhala nzeru ya kwa Mulungu, kwa ife,
kunena kuti kulungama kwathu, chiyero ndi chipulumutso. 31 Choncho
poti zinalembedwa kuti, "Ngati munthu akufuna kunyadira, anyadire
mwa Ambuye."

# 2

1 Pamene ndinabwera kwa inu, abale, sindinabwere ndi luntha lodziwa
kuyankhula kapena nzeru zapamwamba pamene ndinachitira umboni
chinsinsi cha Mulungu. 2 Pakuti ndinatsimikiza pamene ndinali ndi inu
kuti ndisadziwe kanthu kena kupatula Yesu Khristu wopachikidwayo.
3 Ndinabwera kwa inu wofowoka ndi wamantha, ndiponso wonjenjemera
kwambiri. 4 Uthenga ndi ulaliki wanga sunali wa mawu anzeru ndi
onyengerera koma woonetsa mphamvu za Mzimu, 5 kuti chikhulupiriro
chanu chisatsamire pa nzeru ya anthu koma pa mphamvu za Mulungu.

### *Nzeru Yochokera kwa Mzimu*

6 Komabe ife timayankhula uthenga wa nzeru kwa okhwima, koma
osati ndi nzeru ya m'bado uno kapena ya olamula a m'bado uno, amene
mphamvu yawo ikutha. 7 Ayi, ife timayankhula za nzeru yobisika ya
Mulungu, nzeru imene inabisidwa ndipo imene Mulungu anatikonzera
mu ulemerero wathu isanayambe nthawi. 8 Palibe olamulira aliyense
wa m'bado uno amene anamumvetsetsa popeza anakamumvetsetsa
sakanamupachika Ambuye wa ulemerero. 9 Komabe monga zalembedwa
kuti,

"Palibe diso linaona,
    palibe khutu linamva,
palibe amene anaganizira,
    zimene Mulungu anakonzera amene amukonda"

10 koma Mulungu waululira ife mwa Mzimu wake.

Mzimu amafufuza zinthu zonse, ndi zozama za Mulungu zomwe. 11 Kodi
ndani mwa anthu angadziwe maganizo a munthu wina, kupatula mzimu
wa munthuyo wokhala m'kati mwake? Chimodzimodzinso palibe amene
adziwa maganizo a Mulungu kupatula Mzimu wa Mulunguyo. 12 Mzimu

amene tinalandira ife si wa dziko lapansi koma Mzimu wochokera
kwa Mulungu wotipatsa ife mwaulere. 13 Izi ndi zimene timayankhula
osati m'mawu wophunzitsidwa ndi nzeru za munthu koma m'mawu
wophunzitsidwa ndi Mzimu, kufotokozera zoonadi zauzimu m'mawu
auzimu. 14 Munthu wopanda Mzimu savomereza zinthu zimene zichokera
kwa Mzimu wa Mulungu, popeza ndi zopusa kwa iyeyo, ndipo sangaz-
imvetsetse chifukwa zimazindikirika mwa Mzimu. 15 Munthu wauzimu
amaweruza pa zinthu zonse, koma iye mwini saweruzidwa ndi munthu
aliyense. 16 Pakuti
"Ndani anadziwa malingaliro a Ambuye,
    kuti akhoza kumulangiza Iye."
Koma tili nawo mtima wa Khristu.

# 3

*Mpingo ndi Atsogoleri Ake*

1 Ndipo abale sindikanakuyankhulani ngati auzimu koma adziko la-
pansi, makanda chabe mwa Khristu. 2 Ndinakupatsani mkaka osati
chakudya cholimba pakuti munali musanakonzeke kuchilandira. Zoonadi,
simunakonzekebe. 3 Mukanali adziko lapansi. Pakuti pakati panu pali
kaduka ndi kukangana, kodi si inu a dziko lapansi? Kodi simukuchita
ngati anthu wamba? 4 Pamene wina anena kuti, "Ine ndimatsatira Paulo,"
ndipo wina akuti, "Ine ndimatsatira Apolo," Kodi si inu akunja?

5 Ndiponso kodi Apolo ndi ndani? Nanga Paulo ndi ndani? Otumikira
chabe, omwe kudzera mwa iwo inu munakhulupirira monga Ambuye
anawagawira aliyense ntchito yake. 6 Ine ndinadzala mbewu, Apolo
anayithirira, koma Mulungu ndiye anayikulitsa. 7 Choncho kuphatikiza
iye wodzala ndi iye wothirira, onse sali kanthu, koma Mulungu yekha
amene amakulitsa zinthu. 8 Munthu wodzala ndi munthu wothirira ali
ndi cholinga chimodzi, ndipo aliyense adzapatsidwa mphotho molingana
ndi ntchito yake. 9 Pakuti ife ndife antchito anzake a Mulungu; inu ndinu
munda wa Mulungu, Nyumba ya Mulungu.

10 Mwachisomo chimene Mulungu wandipatsa, ine ndinayika maziko
monga mmisiri waluntha, ndipo ena akumangapo. Koma aliyense ayenera
kuchenjera mmene akumangira. 11 Pakuti wina sangayikenso maziko
ena oposera amene anakhazikitsidwa kale, amene ndi Yesu Khristu.
12 Ngati munthu aliyense amanga pa maziko awa pogwiritsa ntchito golide,
siliva, miyala yamtengowapatali, milimo yamitengo, tsekera kapena udzu,
13 ntchito yake idzaonekera pamene Tsiku la chiweruzo lidzazionetsa
poyera. Tsikulo lidzafika ndi moto, ndipo motowo ndi umene udzayesa
ntchito ya munthu aliyense. 14 Ngati zimene zamangidwazo sizidzagwa,
adzalandira mphotho yake. 15 Ndipo ngati zidzanyeke ndi moto, sadza-
landira mphotho koma iye mwini adzapulumukabe, koma monga ngati
munthu amene wapulumuka m'moto.

16 Kodi inu simukudziwa kuti ndinu Nyumba ya Mulungu ndipo kuti
Mzimu wa Mulungu amakhala mwa inu? 17 Ngati wina aliyense awononga
Nyumba ya Mulunguyo, Mulungu nayenso adzamuwononga ameneyo;
popeza Nyumba ya Mulungu ndi yopatulika ndipo Nyumbayo ndi inu
amene.

18 Choncho musadzinyenge. Ngati wina wa inu akuganiza kuti ndi
wanzeru pa mulingo wa m'bado uno, ayenera kukhala "wopusa" kuti athe
kukhala wanzeru. 19 Pakuti nzeru ya dziko lapansi ndi yopusa pamaso

pa Mulungu. Monga kwalembedwera kuti, “Iye amakola anthu ochenjera
mu msampha wa kuchenjera kwawo,” 20 ndiponso, “Ambuye amadziwa
kuti maganizo a wanzeru ndi opandapake.” 21 Choncho, wina asanyadire
anthu chabe! Zonse ndi zanu, 22 kaya Paulo kapena Apolo kapena Kefa
kapena dziko lapansi, kapena moyo, kapena imfa, kapena tsopano, kapena
m’tsogolo, zonse ndi zanu, 23 ndipo inu ndinu a Khristu, ndipo Khristu ndi
wa Mulungu.

# 4

*Atumiki a Khristu*

1 Choncho tsono anthu atione ife monga atumiki a Khristu, ndiponso
ngati osunga zinsinsi za Mulungu. 2 Chofunika kwambiri n’chakuti
amene apatsidwa udindo oyang’anira aonetse kukhulupirika. 3 Ine
ndilibe nazo kanthu ngati ndiweruzidwa ndi inu kapena khothi lina
lililonse. Ndithu, inenso sindidziweruza ndekha. 4 Chikumbumtima
changa sichikunditsutsa, koma sikuti ndine wolungama. Wondiweruza ine
ndi Ambuye. 5 Chomwecho musaweruze nthawi yoweruza isanakwane.
Dikirani mpaka Ambuye atabwera. Iye adzaonetsa poyera zimene zabisika
mu mdima ndipo adzaonetsa maganizo a m’mitima ya anthu. Pa nthawi
imeneyo aliyense adzalandira kwa Mulungu chiyamiko.

6 Tsono abale, ndapereka chitsanzo cha ine mwini ndi Apolo kuti
mupindule. Phunzirani kwa ife tanthauzo la mawu akuti, “Musamapitirire
zimene Malemba akunena,” kuti musamanyade pamene wina aposa
mnzake. 7 Pakuti ndani amakusiyanitsani ndi wina aliyense? N’chiyani
muli nacho chimene simunalandire? Ndipo ngati munalandira, bwanji
mumadzitukumula ngati kuti simunalandire?

8 Inu muli nazo kale zonse zimene mufuna! Inu mwalemera kale! Inu
mwayamba kale kulamulira ife! Ndilakalaka mukanakhaladi mafumu kuti
ife tikhale nawo mafumu pamodzi ndi inu. 9 Pakuti kwa ine zikuoneka
ngati kuti Mulungu watiyika ife atumwi pachionetsero, kumapeto kwa
mndandanda, monga anthu oweruzidwa kuti akaphedwe m’mabwalo. Ife
tayikidwa kuti tionekere ku dziko lonse, kwa angelo ndi anthu. 10 Ife
ndife opusa chifukwa cha Khristu, koma inu ndinu anzeru mwa Khristu!
Ife ndife ofowoka koma inu ndinu amphamvu! Inu ndinu olemekezeka
koma ife ndife opeputsidwa! 11 Mpaka pano tili ndi njala ndi ludzu, tili
ndi sanza, tikuzunzidwa, tilibe nyumba. 12 Timagwira ntchito molimbika
ndi manja athu. Akamatitemberera, ife timadalitsa; tikasautsidwa, ife
timapirira. 13 Pamene atilalatira timayankha mwachifundo. Mpaka pano
takhala ngati zinyalala za dziko, monga zakudzala za dziko lapansi.

*Pempho ndi Chenjezo*

14 Sindikulemba izi kuti ndikuchititseni manyazi, koma kukuchenjezani
monga ana anga okondedwa. 15 Ngakhale muli ndi anthu 10,000 okutso-
golerani mwa Khristu, mulibe abambo ambiri, popeza mwa Khristu Yesu,
ine ndakhala abambo anu kudzera mu Uthenga Wabwino. 16 Chifukwa
chake ndikukupemphani kuti munditsanze ine. 17 Chifukwa cha ichi
ndikutumiza kwa inu Timoteyo, mwana wanga amene ndimamukonda,
amene ndi wokhulupirika mwa Ambuye. Adzakukumbutsani inuyo
za moyo wanga mwa Khristu Yesu, umene ukugwirizana ndi zimene
ndimaphunzitsa paliponse mu mpingo uliwonse.

18 Ena mwa inu mukudzitukumula, ngati kuti sindingabwere kwanu.
19 Koma ndibwera kwanuko posachedwapa, ngati Ambuye alola, ndipo ndi
pamene ndidzadziwe osati zimene anthu odzitukumulawa akuyankhula,
koma kuti mphamvu zawo n'zotani. 20 Pakuti ufumu wa Mulungu si mawu
chabe koma mphamvu. 21 Kodi musankha chiyani? Kodi ndidzabwere ndi
chikwapu, kapena mu chikondi ndiponso mwa mzimu wofatsa?

# 5

### *Wachigololo Achotsedwe mu Mpingo*

1 Mbiri yamveka kuti pakati panu pakuchitika chigololo. Ndipo chigololo
cha mtunduwu ngakhale pakati pa akunja sichingapezeke; munthu
akumagonana ndi mkazi wa abambo ake. 2 Ndipo inu mukudzituku-
mulabe. Kodi simukanayenera kudzazidwa ndi chisoni ndipo mukana-
muchotsa pa chiyanjano chanu munthu wochita zimenezi? 3 Ngakhale
sindili nanu m'thupi, ndili nanu mu mzimu. Ndipo ineyo ndapereka
kale chiweruzo pa munthu amene amachita zotere, ngati kuti ndili
komweko. 4 Mukasonkhana mu dzina la Ambuye athu Yesu, ine ndili
nanu mu mzimu, ndipo mphamvu ya Ambuye athu Yesu ili pomwepo,
5 mumupereke munthuyu kwa Satana, kuti chikhalidwe chake cha uchimo
chiwonongedwe ndikuti mzimu wake udzapulumuke pa tsiku la Ambuye.
6 Kudziwa kwanu si kwabwino. Kodi simukudziwa kuti yisiti wochepa
amafufumitsa mphumphu yaufa wonse wa tirigu? 7 Chotsani yisiti wakale
kuti mukhale ndi mphumphu yopanda yisiti, monga inu muli. Pakuti
Khristu, Mwana Wankhosa wa Paska wathu, anaperekedwa nsembe.
8 Choncho, tiyeni tisunge chikondwererochi, osati ndi yisiti wakale,
wowononga ndi woyipa, koma ndi buledi wopanda yisiti, buledi woona
mtima ndi choonadi.
9 Ndakulemberani m'kalata yanga kuti musayanjane nawo anthu
achigololo. 10 Pamenepatu sindikutanthauzatu anthu a dziko lapansi
lino amene ndi achigololo, kapena aumbombo, kapena opeza ndalama
mwachinyengo, kapena opembedza mafano. Kukanatero mukanango-
choka m'dziko lapansi lino. 11 Koma tsopano ndikukulemberani kuti
musayanjane ndi aliyense amene adzitcha m'bale koma ndi wachigololo,
kapena waumbombo, kapena wopembedza mafano, kapena wonamizira
anzake, woledzera kapena wopeza ndalama mwachinyengo. Munthu
wotere ngakhale kudya, osadya naye pamodzi.
12 Kodi ndipindulanji kuti ndiweruze anthu amene si a mu mpingo? Kodi
simuyenera kuweruza iwo amene ali mu mpingo? 13 Mulungu adzaweruza
akunja. "Chotsani woyipayo pakati panu."

# 6

### *Milandu Pakati pa Anthu Okhulupirira*

1 Pamene wina wa inu ali ndi mlandu ndi mnzake, n'chifukwa chiyani
amatengera nkhaniyo kwa anthu akunja kuti akawaweruze m'malo
mopita nayo kwa oyera mtima? 2 Kodi inu simukudziwa kuti anthu
a Mulungu adzaweruza dziko lapansi? Ndipo ngati inu mungaweruze
dziko lapansi, kodi sindinu oyenera kuweruza milandu ing'onoying'ono?
3 Kodi simukudziwa kuti mudzaweruza angelo? Nanga bwanji zinthu za
m'moyo uno! 4 N'chifukwa chake, ngati pali milandu pa zinthu zotere,
sankhani anthu ena kuti akhale oweruza ngakhale alibe udindo mu

mpingo. 5 Ndikunena izi kuti ndikuchitiitseni manyazi. Moti n'kutheka
kuti pakati panu palibe wina wanzeru zokwanira kuti aziweruza mlandu
pakati pa Akhristu? 6 Koma m'malo mwake m'bale atengera ku bwalo la
mlandu m'bale mnzake kukaweruzidwa. Zonsezi pamaso pa akunja!

7 Chokha choti mwakasumirana chikuonetseratu kuti mwagonjetsedwa
kale. Bwanji osangolola kuti ena akulakwireni? Bwanji osan-
golola kuti ena akubereni? 8 M'malo mwake, inuyo ndiye mum-
abera ena ndi kuwalakwira, ndipo mumachita izi kwa abale anu.
9 Kodi simukudziwa kuti munthu woyipa sadzalowa mu ufumu wa
Mulungu? Musanyengedwe: achigololo, kapena opembedza mafano,
kapena achiwerewere, kapena amuna adama, kapena ogonana ndi
amuna okhaokha; 10 kapena akuba, kapena aumbombo, kapena oledzera,
kapena achipongwe, kapena opeza ndalama mwachinyengo sadzalowa
mu ufumu wa Mulungu. 11 Ndipo umu ndi mmene ena mwa inu munalili.
Koma munatsukidwa, munayeretsedwa, munalungamitsidwa m'dzina la
Ambuye Yesu Khristu ndi Mzimu wa Mulungu wathu.

### *Chigololo*

12 Inu mumati, "Ine ndili ndi ufulu wochita chilichonse." Komatu si
zonse zimene n'zothandiza. "Ndili ndi ufulu wochita chilichonse." Koma
sindidzagonjetsedwa ndi chilichonse. 13 Inu mumati, "Chakudya, kwake
n'kulowa m'mimba ndipo mimba ntchito yake n'kulandira chakudyacho."
Koma Mulungu adzawononga zonsezi. Thupi silochitira chigololo, koma
la Ambuye, ndipo Ambuye ndiye mwini thupilo. 14 Mwamphamvu zake
Mulungu anaukitsa Ambuye kwa akufa, ndipo ifenso adzatiukitsa. 15 Kodi
simukudziwa kuti matupi anuwo ndi ziwalo za Khristu mwini? Kodi
tsono ndingatenge ziwalo za Khristu n'kuzisandutsa ziwalo za mkazi
wadama? Zosatheka! 16 Kodi simukudziwa kuti amene amadzipereka
kwa mkazi wadama, iyeyo ndi mkaziyo amasanduka thupi limodzi? Paja
kunalembedwa kuti, "Awiriwo adzakhala thupi limodzi." 17 Koma amene
amadzipereka kwa Ambuye, iyeyo ndi Ambuye amakhala mzimu umodzi.

18 Thawani dama. Machimo onse amene munthu amachita amakhala
kunja kwa thupi lake, koma amene amachita machimo okhudza chigololo,
amachimwira thupi lake lomwe. 19 Kodi simukudziwa kuti thupi lanu
ndi Nyumba ya Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene mwalandira
kuchokera kwa Mulungu? Inu simuli panokha ayi. 20 Ndinu ochita
kugulidwa. N'chifukwa chake lemekezani Mulungu m'thupi lanu.

# 7

### *Ukwati*

1 Tsopano pa zinthu zomwe munandilembera n'kwabwino kuti munthu
asakwatire. 2 Koma chifukwa choti chigololo chawanda, mwamuna
aliyense akhale naye mkazi wakewake ndipo mkazi aliyense akhale naye
mwamuna wakewake. 3 Mwamuna akwaniritse udindo wake wa pa
banja kwa mkazi wake, ndipo chimodzimodzi mkazi kwa mwamuna
wake. 4 Thupi la mkazi wokwatiwa si la iye mwini yekha koma ndi la
mwamuna wakenso. Momwemonso, thupi la mwamuna si la iye mwini
yekha koma ndi la mkazi wakenso. 5 Musamakanizane, pokhapokha
mutagwirizana awiri kuti mwakanthawi mudzipereke kumapemphero.
Kenaka mukhalirenso pamodzi kuopa kuti Satana angakuyeseni chifukwa
cholephera kudziretsa. 6 Ndikunena zimenezi mokulolani chabe osati

mokulamulani. [7] Ine ndikanakonda anthu akanakhala ngati ine. Koma
poti munthu aliyense ali ndi mphatso yakeyake yochokera kwa Mulungu,
wina mphatso yake, wina yakenso.

[8] Tsono kwa osakwatira onse, ndi akazi amasiye ndikuti, ndi bwino
kwa iwo kukhala osakwatira monga mmene ndilili inemu. [9] Koma ngati
sangathe kudziretsa, akwatire, popeza ndi bwino kukwatira kusiyana ndi
kudzizunza ndi chilakolako.

[10] Kwa amene ali pa banja ndikupatsani lamulo ili (osati langa koma
la Ambuye): Mkazi asalekane ndi mwamuna wake. [11] Koma ngati
atatero, asakwatiwenso, apo ayi, abwerere kwa mwamuna wakeyo. Ndipo
mwamuna asaleke mkazi wake.

[12] Kwa ena onse ndikunena izi (ineyo osati Ambuye); ngati m'bale wina
ali ndi mkazi wosakhulupirira ndipo mkaziyo walola kukhala pa banja
ndi m'baleyo, ameneyo asamuleke. [13] Ngati mayi wina ali ndi mwamuna
wosakhulupirira ndipo mwamunayo walola kukhala pa banja ndi mayiyo,
ameneyo asamuleke. [14] Pakuti mwamuna wosakhulupirirayo amay-
eretsedwa chifukwa cha mkazi wakeyo, ndipo mkazi wosakhulupirira
amayeretsedwa chifukwa cha mwamuna wokhulupirirayo. Kupanda apo
ana anu akanakhala odetsedwa, koma mmene zililimu ndi oyeretsedwa.

[15] Koma ngati wosakhulupirira achoka, mulekeni achoke. Zikatero
ndiye kuti mwamuna kapena mkazi wokhulupirirayo sali womangikanso.
Mulungu anatiyitana kuti tikhale mu mtendere. [16] Kodi iwe, mkazi,
ungadziwe bwanji kuti mwina n'kupulumutsa mwamuna wako? Kapena
iwe, mwamuna, ungadziwe bwanji kuti mwina n'kupulumutsa mkazi
wako?

### *Kukhala Moyo Wosinthika*

[17] Koma aliyense akhale moyo umene Ambuye anamupatsa, umene
Mulungu anamuyitanira. Ili ndiye lamulo limene ndalikhazikitsa
m'mipingo yonse. [18] Ngati pamene munthu amayitanidwa anali atachita
mdulidwe, asavutike n'kubisa za mdulidwe wakewo. Ngatinso pamene
munthu amayitanidwa n'kuti asanachite mdulidwe, asachite mdulidwe.
[19] Mdulidwe si kanthu, kusachita mdulidwe si kanthunso. Chofunika
n'kusunga malamulo a Mulungu. [20] Aliyense akhale monga analili pamene
Mulungu anamuyitana.

[21] Kodi munali kapolo pamene Mulungu anakuyitanani? Musavutike
nazo zimenezi. Koma ngati mutapeza mwayi woti mulandire ufulu,
ugwiritseni ntchito mwayiwo. [22] Pakuti amene anali kapolo pamene
amayitanidwa ndi Ambuye, ndi mfulu wa Ambuye; chimodzimodzinso
amene anali mfulu pamene anayitanidwa, ndi kapolo wa Khristu.
[23] Munagulidwa ndi mtengowapatali, choncho musakhalenso akapolo a
anthu. [24] Abale, aliyense angokhala pamaso pa Mulungu monga momwe
analili pamene Mulungu anamuyitana.

### *Osakwatiwa*

[25] Tsopano za anamwali: Ine ndilibe lamulo lochokera kwa Ambuye,
koma ndipereka maganizo anga monga ngati munthu amene mwachi-
fundo cha Ambuye ndine wodalirika. [26] Chifukwa cha masautso a masiku
ano, ndikuganiza kuti n'kwabwino kuti munthu akhale monga mmene
alili. [27] Kodi ndinu wokwatira? Musalekane. Kodi ndinu wosakwatira?
Musafunefune mkazi. [28] Komabe ngati mukwatira simunachimwe; ndipo
ngati namwali akwatiwa sanachimwenso. Koma amene walowa m'banja

adzakumana ndi zovuta zambiri m'moyo uno, ndipo sindikufuna kuti inu
mukumane ndi zovutazi.
29 Abale, chimene ndikutanthauza n'chakuti nthawi yatha. Kuyam-
bira tsopano anthu okwatira akhale ngati sanakwatire. 30 Amene
akulira akhale monga ngati sakulira. Amene akukondwa akhale ngati
sakukondwa. Amene akugula zinthu akhale ngati alibe zinthuzo.
31 Amene akugwiritsa ntchito zinthu za dziko lapansi lino, akhale ngati
sizikuwakhudza. Pakuti dziko lapansi lino mmene lilirimu, likupita.
32 Ine ndikufuna kuti mumasuke ku nkhawa zanu. Munthu wosakwatira
amangolabadira za Ambuye, mmene angakondweretsere Ambuyewo.
33 Koma wa pa banja amalabadira za dziko lapansi lino, mmene an-
gakondweretsere mkazi wake, 34 ndipo chifukwa ichi amatanganidwa
kwambiri. Mkazi wosakwatiwa kapena namwali, amalabadira za Am-
buye. Cholinga chake ndi kudzipereka kwa Ambuye m'thupi ndi mu
uzimu momwe. Koma mkazi wokwatiwa amalabadira za dziko lapansi
lino, mmene angakondweretsere mwamuna wake. 35 Ndikunena izi
kufuna kuthandiza inu nomwe osati kukupanikizani. Ine ndikufuna
mukhale moyenera mosadzigawa pa kudzipereka kwanu kwa Ambuye.
36 Ngati wina akuganiza kuti akumulakwira namwali yemwe anapalana
naye ubwenzi, ndipo ngati chilakolako chake chikunka chikulirakulirabe,
ndipo akuona kuti n'kofunika kumukwatira, ayenera kuchita monga
wafunira, kutero si kuchimwa ayi. 37 Koma ngati wina motsimikiza
mtima wake, popanda womukakamiza, koma akuchita mwa chifuniro
chake, ndipo watsimikiza mtima kuti samukwatira namwaliyo, munthuyu
akuchitanso chokhoza. 38 Choncho amene akukwatira namwali amene ali
naye pa ubwenzi, akuchita bwino, koma amene sangakwatire namwaliyo
akuchita bwino koposa.
39 Mkazi amamangika ndi lamulo la ukwati nthawi zonse pamene
mwamuna wake ali ndi moyo. Koma mwamuna wake akamwalira,
ali ndi ufulu kukwatiwa ndi wina aliyense amene akumufuna, koma
mwamunayo akhale wa mwa Ambuye. 40 M'maganizo anga, mkaziyo
adzakhala wokondwa koposa ngati atangokhala wosakwatiwa. Ndipo
ndikuganiza kuti inenso ndili naye Mzimu wa Mulungu.

# 8

*Nyama ya Nsembe za Mafano*

1 Tsopano za chakudya choperekedwa nsembe kwa mafano: Ife tidziwa
kuti tonse tili ndi chidziwitso. Komatu chidziwitso chokha chimadzitukumula,
mula, koma chikondi ndicho chimapindulitsa. 2 Munthu amene amaganiza
kuti amadziwa kanthu, ndiye kuti sakudziwa monga mmene amayenera
kudziwira. 3 Koma munthu amene amakonda Mulungu amadziwika ndi
Mulunguyo.
4 Choncho kunena za chakudya choperekedwa nsembe kwa mafano;
ife tikudziwa kuti mafano si kanthu n'pang'onong'ono pomwe pa dziko
lapansi, ndiponso kuti palibe Mulungu wina koma mmodzi yekha.
5 Popeza kuti ngakhale pali yotchedwa milungu, kaya ndi kumwamba
kapena pa dziko lapansi (poti ilipodi milungu yambirimbiri ndi ambuye
ambirimbiri), 6 koma kwa ife pali Mulungu mmodzi yekha, Atate, zinthu
zonse zinachokera mwa Iye ndipo ndife ake. Komanso pali Ambuye
mmodzi Yesu Khristu kumene zinthu zonse zinachokera ndipo mwa Iye
ife tili ndi moyo.

7 Koma saliyense amadziwa zimenezi. Alipo ena ozolowera mafano
kwambiri mwakuti akadya chakudya chotere amaganiza kuti chakudy-
acho chinaperekedwa nsembe kwa mafano. Ndiye poti chikumbumtima
chawo n'chofowoka chimadetsedwadi. 8 Koma chakudya sichitisendeza
kufupi ndi Mulungu. Tikapanda kudya si vuto, tikadya sitisinthikanso.

9 Komabe samalani kuti ufulu wanu ochita zinthu usafike pokhumud-
witsa ofowoka. 10 Pakuti ngati aliyense wachikumbumtima chofowoka
akakuonani achidziwitsonu mukudya m'nyumba yopembedzera mafano,
kodi iyeyo sichidzamulimbitsa mtima kuti azidya chakudya choperekedwa
nsembe kwa mafano? 11 Kotero kuti chifukwa cha chidziwitso chanu
m'bale wofowokayu amene chifukwa cha iye, Khristu anafa, wa-
wonongeka chifukwa cha chidziwitso chanu. 12 Mukamachimwira abale
anu motere ndikuwawonongera chikumbumtima chawo chofowokacho,
mukuchimwira Khristu. 13 N'chifukwa chake ngati zimene ine ndimadya
zichititsa m'bale wanga kugwa mu tchimo, sindidzadyanso chakudyacho
kuti m'baleyo ndisamuchimwitse.

# 9

*Paulo Chitsanzo cha Mtumiki wa Uthenga Wabwino*

1 Kodi sindine mfulu? Kodi sindine mtumwi? Kodi sindinamuone
Ambuye athu Yesu? Kodi inu sindiye zotsatira za ntchito yanga mwa
Ambuye? 2 Ngakhale kwa ena sindingakhale mtumwi, mosakayika ndine
mtumwi kwa inu! Poti inu ndi chizindikiro cha utumwi wanga mwa
Ambuye.

3 Kwa iwo wofuna kundizenga milandu ndimawayankha kuti: 4 Kodi ife
tilibe ulamuliro wakudya ndi kumwa? 5 Kodi ife tilibe ulamuliro wotenga
mkazi wokhulupirira n'kumayenda naye monga amachitira atumwi ena
ndi abale awo a Ambuye ndiponso Kefa? 6 Kodi kapena ine ndekha ndi
Barnaba ndiye tikuyenera kugwira ntchito kuti tipeze zotisowa?

7 Ndani angagwire ntchito ya usilikali namadzipezera yekha zofunika
zonse? Kodi ndani amadzala mpesa koma wosadyako zipatso zake? Ndani
amaweta nkhosa koma wosamwako mkaka wake? 8 Kodi moti zimene
ndikunenazi ndimaganizo a umunthu chabe? Kodi Malamulo sakunena
chimodzimodzinso? 9 Popeza analemba m'Malamulo a Mose kuti,
"Musamange ng'ombe pakamwa pamene ikupuntha tirigu." Kodi pamene
Mulungu ananena zimenezi ankalabadira za ng'ombe zokha? 10 Ndithu
Iyeyo amanena za ifenso, kodi si choncho? Inde, izi anazilemba chifukwa
cha ife, pakuti wolima ndiponso wopuntha, onsewo amagwira ntchito
mwachiyembekezo chodzagawana zokololazo. 11 Ngati tidzala mbewu
yauzimu pakati panu, kodi ndi chovuta kwambiri kuti tikolole zosowa
zathu kuchokera kwa inu? 12 Ngati ena ali ndi ufulu wothandizidwa ndi
inu, kodi ife sitikuyenera kukhala nawo ufulu ochulukirapo?

Koma ife sitinagwiritse ntchito ufulu umenewu. M'malo mwake
timangodzichitira chilichonse posafuna kutsekereza ena kumva Uthenga
Wabwino wa Khristu.

13 Kodi simukudziwa kuti wogwira ntchito m'Nyumba ya Mulungu
amapeza chakudya chawo m'Nyumbamo, ndipo kuti otumikira pa
guwa lansembe amagawana zimene zaperekedwa pa guwa lansembelo.
14 Chomwechonso Ambuye akulamula kuti wolalikira Uthenga Wabwino
azilandira thandizo lawo polalikira Uthenga Wabwinowo.

15 Koma ine sindinagwiritse ntchito ufulu woterewu. Sindikulemba izi
ndi chiyembekezo choti mundichitire zoterezi. Kuli bwino ndife kusiyana
n'kuti wina alande zomwe ndimazinyadira. 16 Komatu ndikamalalikira
Uthenga Wabwino, sindingadzitamandire popeza ndimawumirizidwa ku-
lalikira. Tsoka kwa ine ngati sindilalikira Uthenga Wabwino! 17 Ngati
ndikugwira ntchitoyi mwakufuna kwanga, ndili ndi mphotho; koma ngati
si mwakufuna kwanga, ndiye kuti ntchitoyi ndi Ambuye anandipatsa.
18 Tsono mphotho yanga ndi chiyani? Ndi iyi: kuti polalikira Uthenga
Wabwino ndiwupereke kwaulere komanso kuti ndisagwiritse ntchito
ufulu wanga polalikira uthengawo.

### *Ufulu wa Paulo*

19 Ngakhale ndine mfulu ndipo sindine kapolo wa munthu, ndi-
madzisandutsa kapolo wa aliyense kuti ndikope ambiri mmene ndin-
gathere. 20 Kwa Ayuda ndimakhala ngati Myuda kuti ndikope Ayuda.
Kwa olamulidwa ndi Malamulo ndimakhala ngati wolamulidwa nawo
(ngakhale kuti sindine wolamulidwa ndi Malamulowo) kuti ndikope
amene amalamulidwa ndi Malamulo. 21 Kwa amene alibe Malamulo ndi-
makhala wopanda Malamulo (ngakhale kuti sindine wopanda Malamulo a
Mulungu koma ndili pansi pa ulamuliro wa Khristu) kuti ndikope wopanda
Malamulo. 22 Kwa ofowoka ndimakhala wofowoka, kuti ndikope ofowoka.
Ndimachita zinthu zilizonse kwa anthu onse kuti mwanjira ina iliyonse
ndipulumutse ena. 23 Ndimachita zonsezi chifukwa cha Uthenga Wabwino,
kuti ndigawane nawo madalitso ake.

### *Kufunika kwa Kudziretsa*

24 Kodi simukudziwa kuti pa mpikisano wa liwiro onse amathamanga
ndithu, koma mmodzi yekha ndiye amalandira mphotho? Motero thaman-
gani kuti mupate mphotho. 25 Aliyense wochita mpikisano amakonzekera
mwamphamvu. Amachita izi kuti alandire mphotho yankhata yamaluwa
yomwe imafota. Koma ife timachita izi kuti tilandire mphotho yosafota.
26 Choncho sindithamanga monga wothamanga wopanda cholinga; ko-
manso sindichita mpikisano wankhonya monga munthu amene aman-
gomenya mophonya. 27 Ine ndimazunza thupi langa ndi kulisandutsa
kapolo kuti nditatha kulalikira ena, ineyo ndingadzapezeke wosayenera
kulandira nawo mphotho.

## 10

### *Chenjezo Kuchokera M'mbiri ya Israeli*

1 Pakuti sindikufuna kuti inu mukhale osadziwa zenizeni, abale,
kuti makolo athu anatsogozedwa ndi mtambo ndikuti onse anawoloka
nyanja. 2 Ndipo onse anabatizidwa mwa Mose mu mtambo ndi m'nyanja.
3 Onse anadya chakudya chimodzi chauzimu 4 ndipo anamwa chakumwa
chimodzi chauzimu; popeza anamwa kuchokera m'thanthwe lomwe
anayenda nalo, ndipo thanthwe limeneli linali Khristu. 5 Ngakhale zinali
choncho, Mulungu sanakondwere ndi ambiri a iwo, motero ambiri mwa
iwo anafera m'chipululu.
6 Tsono zinthu izi zinachitika kuti zikhale chitsanzo, kuti ife tisayike
mitima yathu pa zinthu zoyipa monga anachitira makolo athuwo.
7 Musakhale anthu opembedza mafano, monga analili ena mwa iwo.
Pakuti zalembedwa kuti, "Anthuwo anakhala pansi nayamba kudya ndi

kumwa. Kenaka anayimirira nayamba kuvina mwachilendo.” 8 Tisachite
chigololo monga ena mwa iwo anachitira ndipo tsiku limodzi anafapo
anthu 23,000. 9 Tisamuyese Khristu, monga ena mwa iwo anachitira ndipo
anaphedwa ndi njoka. 10 Ndipo osamawiringula, monga ena mwa iwo
anachitira naphedwa ndi mngelo wowononga.

11 Zinthu izi zinawachitikira kuti zikhale chitsanzo ndipo zinalembedwa
kuti zikhale chenjezo kwa ife, amene tiyandikira nthawi ya kutha kwa
zonse. 12 Choncho, ngati mukuganiza kuti mwayima mwamphamvu,
samalani mungagwe! 13 Palibe mayesero amene mwakumana nawo oposa
amene anthu ena onse anakumana nawo. Mulungu ngokhulupirika;
sadzalola kuti inu muyesedwe koposa muyeso umene mutha kupirira.
Koma pamene mwayesedwa, Iyenso adzakupatsani njira yopambanira
mayeserowo.

### *Maphwando a Mafano ndi Mgonero wa Ambuye*

14 Choncho abwenzi anga okondedwa, lekani kupembedza mafano.
15 Ndikuyankhula kwa a anthu anzeru zawo, nokha muweruze pa zimene
ndikunenazi. 16 Pamene tidalitsa chikho cha Mgonero wa Ambuye,
mothokoza Mulungu, kodi sitikugawana magazi a Khristu? Nanga buledi
amene timanyemayo, kodi sitikugawana thupi la Khristu? 17 Pakuti buledi
ndi mmodzi yekha, ifenso ngakhale tili ambiri, ndife thupi limodzi, popeza
tonse timagawana buledi mmodzi yemweyo.

18 Taganizirani zimene amachita Aisraeli. Kodi onse amene amadya
zoperekedwa nsembe, samachita nawo miyambo ya pa guwapo? 19 Kodi
ndikutanthauza kuti nsembe zoperekedwa kwa mafano ndi kanthu konse,
kapena kuti mafano ndi kanthu konse? 20 Ayi. Nsembe za osakhulupirira
zimaperekedwa kwa ziwanda, osati kwa Mulungu, ndipo sindikufuna kuti
muziyanjana ndi ziwandazo. 21 Simungamwe chikho cha Ambuye, ndi
kukamweranso chikho cha ziwanda. Simungadyere pa tebulo la Ambuye
ndiponso la ziwanda. 22 Kodi tikufuna kuwutsa mkwiyo wa Ambuye? Kodi
ndife amphamvu kuposa Iye?

### *Ufulu wa Munthu Wokhulupirira*

23 Mutha kunena kuti, “Zinthu zonse n’zololedwa,” komatu si zonse zili
za phindu. “Zinthu zonse n’zololedwa,” komatu si zonse zimathandiza.
24 Munthu aliyense asafunefune zokomera iye yekha, koma zokomeranso
ena.

25 Idyani nyama iliyonse imene amagulitsa pa msika, osafunsa mafunso
okhudzana ndi chikumbumtima chanu. 26 Popeza kuti, “Dziko lapansi ndi
la Ambuye ndi zonse za m’menemo ndi zake.”

27 Ngati wosakhulupirira akuyitanani kuti mukadye naye, inuyo
ndi kuvomera kupitako, mukadye chilichonse chimene akakupatseni
ndipo musakafunse mafunso okhudzana ndi chikumbumtima chanu.
28 Koma ngati wina akuwuzani kuti, “Izi zaperekedwa nsembe,” mu-
sadye zimenezo, pofuna kuthandiza amene wakuwuzaniyo komanso
chifukwa cha chikumbumtima. 29 Ndikunena za chikumbumtima cha
winayo osati chanu. Tsono mungafunse kuti, n’chifukwa chiyani ufulu
wanga ukuphwanyidwa chifukwa cha chikumbumtima cha munthu wina?
30 Ngati ndikuyamika Mulungu chifukwa cha chakudya, nanga munthu
angandinyoze bwanji pa zinthu zomwe ndayamikira nazo Mulungu?

31 N'chifukwa chake chilichonse mungadye kapena kumwa, kapena
chimene mungachite, chitani zonse ku ulemerero wa Mulungu.
32 Musakhumudwitse aliyense, kaya ndi Myuda, Mgriki, kapena mpingo
wa Mulungu. 33 Mu zonse ndikuyesetsa kukondweretsa aliyense m'njira
iliyonse. Popeza sindikufunafuna zokondweretsa ine ndekha koma
zokomera ambiri kuti apulumutsidwe.

# 11

1 Tsatirani chitsanzo changa, monga inenso nditsatira chitsanzo cha
Khristu.

### *Makhalidwe Oyenera pa Mapemphero*

2 Ndikukuyamikani chifukwa chondikumbukira pa zonse ndiponso
posunga ziphunzitso monga ndinakuphunzitsirani. 3 Tsopano ndiku-
funa muzindikire kuti Khristu ndiye mutu wa munthu aliyense, ndipo
mwamuna ndiye mutu wamkazi, ndipo mutu wa Khristu ndi Mulungu.
4 Mwamuna aliyense wopemphera kapena kunenera ataphimba mutu
wake akunyoza mutu wakewo. 5 Ndipo mkazi aliyense wopemphera
kapena kunenera asanaphimbe mutu wake sakulemekeza mutu wakewo.
Kuli chimodzimodzi kumeta mutu wake. 6 Ngati mkazi saphimba kumutu
kwake, ndiye kuti amete tsitsi lake. Ngati n'chamanyazi kwa mkazi
kungoyepula kapena kumeta mpala, ndiye kuti aphimbe kumutu kwake.
7 Mwamuna sayenera kuphimba kumutu popeza ndi chifaniziro ndi
ulemerero wa Mulungu; pamene mkazi ndi ulemerero wa mwamuna.
8 Pakuti mwamuna sachokera kwa mkazi, koma mkazi kwa mwamuna.
9 Ndipo mwamuna sanalengedwe chifukwa cha mkazi, koma mkazi
analengedwera mwamuna. 10 Pa chifukwa ichi, ndiponso pa chifukwa cha
angelo, mkazi akuyenera kukhala ndi chizindikiro cha ulamuliro wake.
11 Komabe mwa Ambuye, mkazi amadalira mwamuna ndipo mwamuna
amadalira mkazi. 12 Pakuti monga mkazi anachokera kwa mwamuna,
momwemonso mwamuna anabadwa mwa mkazi. Koma zonse zichokera
kwa Mulungu.
13 Dziweruzeni. Kodi n'chabwino kuti mkazi apemphere kwa Mulungu
wopanda chophimba kumutu? 14 Kodi chikhalidwe chathu sichitiphunz-
itsa kuti n'chamanyazi kuti mwamuna akhale ndi tsitsi lalitali, 15 koma
mkazi akakhala ndi tsitsi lalitali ndi ulemerero wake? Pakuti mkazi
anapatsidwa tsitsi lalitali monga chophimba kumutu. 16 Ngati wina
akufuna kutsutsapo pa zimenezi, ife ndiponso mipingo ya Mulungu tilibe
machitidwe ena apadera koma ndi omwewa.

### *Mgonero wa Ambuye*

17 Koma popereka malangizo awa sindikufuna kukuyamikirani popeza
m'misonkhano yanu mumachita zoyipa kuposa zabwino. 18 Choyamba,
ndikumva kuti mukasonkhana mu mpingo mumasankhana ndipo
ndikukhulupirira kuti zimenezi kwinaku n'zoona. 19 N'zosakayikitsa kuti
pali kugawikana pakati panu kuti adziwike amene ndi ovomerezeka
ndi Mulungu. 20 Tsono, mukasonkhana pamodzi, chimene mumadya si
Mgonero wa Ambuye. 21 Pakuti mukamadya, aliyense amangodzidyera
zomwe anakonza. Wina amakhala ndi njala pamene wina amaledzera.
22 Kodi mulibe nyumba zanu kumene mungamadyere ndi kumwa?
Kapena mumapeputsa mpingo wa Mulungu ndi kuchititsa manyazi amene

alibe kalikonse? Ndikunena chiyani kwa inu? Moti ndikuyamikireni pa zimenezi? Ayi, pa zinthu izi sindingakuyamikireni.

23 Pakuti zimene ndinalandira kwa Ambuye ndi zomwe ndinaku-
patsani. Ambuye Yesu, usiku umene anaperekedwa uja, anatenga
buledi. 24 Atayamika ndi kumunyema ananena kuti, "Ili ndi thupi langa
lomwe laperekedwa kwa inu; muzichita zimenezi pokumbukira Ine."
25 Chimodzimodzi, atatha kudya, anatenga chikho, nati, "Chikho ichi ndi
pangano latsopano la magazi anga; imwani nthawi zonse pokumbukira
Ine." 26 Pakuti nthawi zonse pamene mudya bulediyu ndikumwa
chikhochi, mukulalikira imfa ya Ambuye mpaka Iye adzabweranso.

27 Chifukwa chake, aliyense amene adya buledi kapena kumwa
chikho cha Ambuye m'njira yosayenera adzachimwira thupi ndi magazi
a Ambuye. 28 Munthu adzisanthule yekha asanadye buledi kapena
kumwa chikhochi. 29 Popeza aliyense amene adya kapena kumwa
mosazindikira thupi la Ambuye, amadya ndi kumwa chiweruzo chake
chomwe. 30 N'chifukwa chake pakati panu ambiri mwa inu ndi ofowoka
ndi odwala, ndipo ambirinso agona tulo. 31 Koma tikanadziyesa tokha
sitikaweruzidwanso. 32 Pamene tiweruzidwa ndi Ambuye, ndiye kuti
akukonza khalidwe lathu kupewa kuti tingatsutsidwe pamodzi ndi anthu osakhulupirira.

33 Ndiye tsono abale anga, pamene musonkhana pa chakudya, mudikiri-
rane. 34 Ngati wina ali ndi njala, adye ku nyumba kwake kuti pamene
musonkhana pamodzi zisafike poti muweruzidwe nazo.

Ndipo ndikabwera ndidzakupatsani malangizo ena owonjezera.

# 12

### *Mphatso za Mzimu Woyera*

1 Tsopano abale anga okondedwa, sindikufuna mukhale osadziwa za
mphatso za Mzimu. 2 Inu mukudziwa kuti pamene munali akunja,
ankakusocheretsani m'njira zosiyanasiyana ndi kukukokerani ku mafano
osayankhula. 3 N'chifukwa chake ndikuwuzani kuti palibe munthu amene
ali ndi Mzimu wa Mulungu angayankhule kuti, "Yesu atembereredwe," ndiponso palibe munthu anganene kuti "Yesu ndi Ambuye," popanda kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

4 Pali mphatso zosiyanasiyana, koma Mzimu yemweyo. 5 Pali mautumiki
osiyanasiyana koma Ambuye yemweyo. 6 Pali magwiridwe antchito
osiyanasiyana, koma Mulungu yemweyo amagwira ntchito monsemo mwa anthu onse.

7 Tsono Mzimu amapereka mphatso kwa aliyense kuti ipindulire
onse. 8 Mzimu amapereka kwa munthu wina mawu anzeru, Mzimu
yemweyonso amapereka kwa wina mawu achidziwitso. 9 Kwa wina,
Mzimu yemweyo amapereka chikhulupiriro, kwa wina mphatso za-
machiritso, Mzimu yemweyo. 10 Kwa wina mphamvu zochita zodabwitsa,
kwa wina mawu a uneneri, kwa wina mphatso yozindikira mizimu,
kwa wina malilime osiyanasiyana, ndiponso kwa wina kutanthauzira
malilimewo. 11 Zonsezi ndi ntchito za Mzimu mmodzi yemweyo, ndipo
amapereka kwa munthu aliyense monga momwe Mzimuyo wafunira.

### *Thupi Limodzi Ziwalo Zambiri*

12 Thupi ndi limodzi, ngakhale kuti lapangidwa ndi ziwalo zambiri.
Ndipo ngakhale ziwalo zake zonse ndi zambiri, zimapanga thupi limodzi.

Momwemonso ndi mmene alili Khristu. 13 Pakuti tonse tinabatizidwa
ndi Mzimu mmodzi m'thupi limodzi. Myuda kapena Mgriki, kapolo
kapena mfulu tonse tinapatsidwa kuti timwe Mzimu mmodzi yemweyo.
14 Tsopano thupi silinapangidwe ndi chiwalo chimodzi koma ndi ziwalo
zambiri.

15 Ngati phazi litanena kuti, "Pakuti sindine dzanja, sindine chiwalo
cha thupi." Chifukwa chimenechi sichingachititse phazi kuti lisakhale
chiwalo cha thupi. 16 Ndipo ngati khutu litanena kuti, "Pakuti sindine
diso, sindine chiwalo cha thupi." Chifukwa chimenechi sichingachititse
khutu kuti lisakhale chiwalo cha thupi. 17 Kodi thupi lonse likanakhala
diso, tikanamamva bwanji? Nanga thupi lonse likanakhala khutu,
tikanamanunkhiza bwanji? 18 Koma zoona n'zakuti, Mulungu anayika
ziwalo m'thupi, chilichonse monga momwe Iye anafunira. 19 Nanga zonse
zikanakhala chiwalo chimodzi, ndiye thupi likanakhala lotani? 20 Mmene
zililimu, pali ziwalo zambiri koma thupi ndi limodzi lokha.

21 Diso silingawuze dzanja kuti, "Iwe sindikukufuna!" Ndipo mutu sun-
gawuze phazi kuti "Iwe sindikukufuna!" 22 M'malo mwake, ziwalo zathupi
zimene zimaoneka ngati zofowoka ndizo zili zofunikira kwambiri, 23 ndipo
ziwalo zathupi zimene timaziyesa zopanda ulemu, ndizo timazilemekeza
kwambiri. Ndipo ziwalo zosaoneka bwino ndizo zimalandira ulemu
wapadera. 24 Koma ziwalo zooneka bwino, n'kosafunika kuti tizisamalire
mwapadera. Mulungu polumikiza ziwalo zathupi, anapereka ulemu
wopambana kwa ziwalo zimene zimafunadi ulemuwo 25 kuti pasakhale
kugawikana m'thupi koma kuti ziwalo zonse zisamalirane. 26 Ngati
chiwalo chimodzi chikumva kuwawa, ziwalo zonse zimamvanso kuwawa.
Ngati chiwalo chimodzi chilandira ulemu, ziwalo zonse zimakondwera
nawo.

27 Tsopano inu ndinu thupi la Khristu, ndipo aliyense wa inu ndi chiwalo
cha thupilo. 28 Ndipo Mulungu mu mpingo anayika poyamba atumwi,
kachiwiri aneneri, kachitatu aphunzitsi, kenaka ochita zozizwitsa, ena a
mphatso zamachiritso, ena a mphatso yothandiza anzawo, ena a mphatso
yotsogolera ndiponso ena a mphatso ya malilime. 29 Kodi onse ndi
atumwi? Kodi onse ndi aneneri? Kodi onse ndi aphunzitsi? Kodi
onse amachita zozizwitsa? 30 Kodi onse ali ndi mphatso zamachiritso?
Kodi onse amayankhula malilime? Kodi onse amatanthauzira malilime?
31 Koma funitsitsani mphatso zopambana.

Tsopano ndikuonetsani njira yopambana kwambiri.

# 13

*Kupambana kwa Chikondi*

1 Ngakhale nditamayankhula m'malilime a anthu ndi a angelo, koma
ngati ndilibe chikondi, ndili ngati chinganga chaphokoso kapena ngati chit-
sulo chosokosera. 2 Ngati ndili ndi mphatso ya uneneri, n'kumazindikira
zinsinsi ndi kudziwa zonse, ndipo ngati ndili ndi chikhulupiriro chosuntha
mapiri, koma wopanda chikondi, ine sindili kanthu. 3 Ngati ndipereka
zanga zonse kwa osauka ndi kupereka thupi langa kuti alitenthe, koma
ngati ndilibe chikondi, ine sindipindula kanthu.

4 Chikondi n'choleza mtima, chikondi n'chokoma mtima, chilibe
nsanje, sichidzikuza, sichidzitamandira. 5 Chikondi chilibe mwano,
sichodzikonda, sichipsa mtima msanga, sichisunga mangawa. 6 Chikondi
sichikondwera ndi zoyipa koma chimakondwera ndi choonadi.

7 Chimatchinjiriza nthawi zonse, chimakhulupirika nthawi zonse,
chimakhala ndi chiyembekezo nthawi zonse, chimapirira nthawi zonse.
8 Chikondi ndi chosatha. Koma mphatso ya uneneri idzatha, pamene pali
kuyankhula malilime adzatha, pamene pali chidziwitso chidzatha. 9 Pakuti
timadziwa zinthu pang'ono chabe ndipo timanenera pang'ono chabe.
10 Koma changwiro chikadzaoneka ndipo choperewerachо chidzatha.
11 Pamene ndinali mwana ndinkayankhula ngati mwana, ndinkaganiza
ngati mwana, ndinkalingalira ngati mwana. Koma nditakula, zonse
zachibwana ndinazisiya. 12 Pakuti tsopano tiona zinthu mosaoneka bwino
ngati m'galasi loonera; kenaka tidzaziona maso ndi maso. Tsopano
ndidziwa mosakwanira koma kenaka ndidzadziwa mokwanira, monga
mmene Mulungu akundidziwira ine.
13 Ndipo tsopano zatsala zinthu zitatu: chikhulupiriro, chiyembekezo
ndi chikondi. Koma chachikulu pa zonsezi ndi chikondi.

# 14

*Mphatso ya Uneneri ndi ya Malilime*

1 Funafunani chikondi, ndikufunitsitsa mphatso zauzimu, makamaka
mphatso ya uneneri. 2 Pakuti aliyense amene amayankhula malilime
sayankhula kwa anthu, koma kwa Mulungu. Zoonadi, palibe amene
amamva zimene akunena chifukwa Mzimu ndiye amamuyankhulitsa
zachinsinsi. 3 Koma amene amanenera amayankhula kwa anthu kuti
awapatse mphamvu, awalimbikitse ndi kuwakhazikitsa mtima pansi.
4 Iye amene amayankhula malilime amadzilimbikitsa yekha, koma amene
amanenera amalimbikitsa mpingo. 5 N'kanakonda kuti aliyense mwa
inu atamayankhula malilime, koma ndi bwino kuti muzinenera. Amene
amanenera amaposa amene amayankhula malilime, pokhapokha atatan-
thauzira kuti mpingo upindule.
6 Tsono, abale, mudzapindula chiyani nditabwera kwa inu ndi
kukuyankhulani m'malilime? Koma mudzapindula ngati nditakub-
weretserani vumbulutso lina lake, kapena chidziwitso, kapena chi-
phunzitso. 7 Ngakhale mu zinthu zopanda moyo monga chitoliro
kapena gitala, zimene zimatulutsa liwu; kodi munthu akhoza kudziwa
bwanji nyimbo imene ikuyimbidwa ngati mawu sakumveka mogwirizana
bwino? 8 Komanso ngati lipenga silimveka bwino, ndani angakonzekere
nkhondo? 9 Chimodzimodzinso inu. Ngati simungayankhule mawu
omveka bwino m'chiyankhulo chanu, wina angadziwe bwanji chimene
mukunena? Muzingodziyankhulira nokha. 10 Mosakayika, pali ziyankhulo
zosiyanasiyana pa dziko lapansi, koma palibe n'chimodzi chomwe
chimene chilibe tanthauzo. 11 Tsono ngati sindingatolepo tanthauzo la
zimene wina akuyankhula, ndiye kuti ndine mlendo kwa oyankhulayo
ndipo iyeyo ndi mlendo kwa ine. 12 Chimodzimodzinso inu. Popeza
mumafunitsitsa mphatso za Mzimu, yesetseni kuchita bwino pa mphatso
zimene zimamanga mpingo.
13 Pa chifukwa ichi munthu amene amayankhula malilime apemphere
kuti azitha kutanthauzira zimene akunena. 14 Popeza ngati ndipemphera
m'malilime, ndi mzimu wanga umene ukupemphera, koma nzeru zanga
sizikupindula kanthu. 15 Tsono pamenepa n'kutani? Ndidzapemphera
ndi mzimu wanga, komanso ndidzapemphera ndi nzeru zanga. Ndidza-
yimba ndi mzimu wanga, komanso ndidzayimba ndi nzeru zanga.
16 Ngati mutamanda Mulungu mu mzimu, kodi munthu amene wapezeka

pakati pa amene akuyankhula zomwe sakumva, adzavomereza bwanji
kuti "Ameni" pa pemphero lanu loyamikalo popeza sakumva chimene
mukunena? 17 Mukhoza kumathokoza mokwanira, koma munthu winayo
sanathandizikepo.
18 Ndikuyamika Mulungu chifukwa ndimayankhula malilime kuposa
nonsenu. 19 Koma mu mpingo ndi kwabwino kuti ndiyankhule
mawu asanu okha omveka bwino kuti ndilangize bwino ena kusiyana
ndikuyankhula mawu ambirimbiri m'malilime.
20 Abale, lekani kuganiza ngati ana. Mukhale ana pa nkhani ya zoyipa
koma m'maganizo anu mukhale okhwima. 21 Zinalembedwa m'Malamulo
kuti,

"Ndidzayankhula kwa anthu awa,
kudzera mwa anthu aziyankhulo zachilendo
ndiponso ndi milomo yachilendo.
Koma ngakhale nthawi imeneyo sadzandimvera Ine,
akutero Ambuye."

22 Kotero, malilime ndi chizindikiro, osati cha kwa okhulupirira koma
kwa osakhulupirira. Koma kunenera ndi chizindikiro kwa okhulupirira
osati kwa osakhulupirira. 23 Kotero kuti ngati mpingo wonse utasonkhana
pamodzi ndipo aliyense namayankhula malilime, ndipo wina amene
sangazindikire kapena ena osakhulupirira nabwerapo, kodi sadzanena
kuti mwachita misala? 24 Koma ngati wosakhulupirira kapena wina
amene sakuzindikira abwera pamene aliyense akunenera, adzatsutsika
mu mtima ndi zonse zimene akumva ndipo adzaweruzidwa ndi onse
25 ndipo zinsinsi za mu mtima mwake zidzawululika. Kotero kuti
adzadzigwetsa pansi ndi kupembedza Mulungu akufuwula kuti, "Mulungu
ali pakati panudi!"

### *Kupembedza Mwadongosolo*

26 Kodi tsono abale, tinene chiyani? Pamene musonkhana pamodzi,
aliyense amakhala ali ndi nyimbo yoti ayimbe, kapena mawu oti alangize,
vumbulutso, malilime, kapena kumasulira kwake. Zonsezi cholinga
chake chikhale kulimbikitsa mpingo. 27 Ngati wina ayankhula malilime,
awiri kapena akachulukapo atatu ndiye ayankhule mmodzimmodzi, ndipo
wina ayenera kutanthauzira zimene ayankhulazo. 28 Ngati palibe wotan-
thauzira, woyankhulayo akhale chete mu mpingo ndipo adziyankhulire
iye mwini ndi Mulungu.
29 Aneneri awiri kapena atatu anenere, ndipo enawo asanthule
mosamalitsa zimene anenerazo. 30 Ndipo ngati vumbulutso labwera
kwa munthu amene wakhala pansi, amene akuyankhulayo akhale chete.
31 Pakuti nonse mukhoza kunenera mmodzimmodzi motsatana kuti
aliyense alangizidwe ndi kulimbikitsidwa. 32 Mizimu ya aneneri imamvera
ulamuliro wa aneneri. 33 Pakuti Mulungu si Mulungu wachisokonezo
koma wamtendere. Monga mwa mipingo yonse ya oyera mtima.

### *Amayi Akhale Chete mu Mpingo*

34 Amayi akhale chete m'misonkhano ya mpingo. Iwo asaloledwe
kuyankhula, koma azikhala omvera monga mmene lamulo linenera.
35 Ngati ali ndi mafunso, akafunse amuna awo ku nyumba. N'chochititsa
manyazi kuti mkazi ayankhule mu msonkhano wa mpingo.
36 Kodi kapena mawu a Mulungu anachokera kwa inu? Kapena anafika
kwa inu nokha? 37 Ngati wina aliyense akuganiza kuti ndi mneneri
kapena kuti ali ndi mphatso za Mzimu, ayenera kudziwa kuti zimene

ndikukulemberanizi ndi lamulo la Ambuye. 38 Ngati munthu savomereza
zimenezi, iyeyonso sadzavomerezedwa.
39 N'chifukwa chake, abale anga, funitsitsani kunenera, ndipo musaletse
anthu kuyankhula malilime. 40 Koma chilichonse chichitike moyenera ndi
mwadongosolo.

# 15

### *Za Kuuka kwa Khristu*

1 Tsono abale, ndikufuna ndikukumbutseni za Uthenga Wabwino umene
ndinakulalikirani. Munawulandira ndipo munawukhulupirira kolimba.
2 Inu munapulumutsidwa ndi Uthenga Wabwinowu, ngati mwasunga
mawu amene ndinakulalikirani. Kupanda kutero, mwangokhulupirira
pachabe.
3 Pakuti chimene ndinalandira ndinapereka kwa inu monga chofunika
kuposa zonse, kuti Khristu anafera zoyipa zathu monga mwa Malemba,
4 kuti anayikidwa m'manda, kuti anaukitsidwa tsiku lachitatu monga mwa
Malemba; 5 ndipo kuti anaonekera kwa Petro, ndipo kenaka kwa Atumwi
khumi ndi awiriwo. 6 Pambuyo pake, Iye anaonekera kwa anthu oposa 500
mwa abale pa nthawi imodzi, ndipo ambiri mwa iwo akanali ndi moyo
ngakhale kuti ena anagona tulo. 7 Kenaka anaonekeranso kwa Yakobo,
kenaka kwa atumwi onse. 8 Potsiriza pa onse anaonekeranso kwa ine,
monga mwana wobadwa nthawi isanakwane.
9 Pakuti ine ndine wamng'ono kwa atumwi ndipo sindiyenera n'komwe
kutchedwa mtumwi chifukwa ndinazunza mpingo wa Mulungu. 10 Koma
mwachisomo cha Mulungu, ndili mmene ndililimu, ndipo chisomo chake
kwa ine sichinali chopanda ntchito. Ndinagwira ntchito kuposa ena onse
a iwo. Choncho sindine koma chisomo cha Mulungu chimene chinali ndi
ine. 11 Tsono kaya ndi ineyo kapena iwowo, izi ndi zomwe timalalikira,
ndipo izi ndi zimene munakhulupirira.

### *Kuuka kwa Oyera Mtima*

12 Koma ngati timalalikira kuti Khristu anaukitsidwa kwa akufa,
zikutheka bwanji kuti ena mwa inu azinena kuti kulibe kuuka kwa
akufa? 13 Ngati kulibe kuuka kwa akufa, ndiye kuti ngakhale Khristu
sanaukenso. 14 Ndipo ngati Khristu sanaukitsidwe, ndiye kuti kulalikira
kwathu n'kopanda ntchito, ndipo chikhulupiriro chanu n'chopandanso
ntchito. 15 Kuwonjezera pamenepa, ndiye kuti ndife mboni zabodza pa
za Mulungu, pakuti tikuchita umboni kuti Mulungu anaukitsa Khristu
kwa akufa. Ngati n'zoona kuti akufa saukitsidwa, ndiye kuti Mulungu
sanaukitsenso Khristu. 16 Pakuti ngati akufa saukitsidwa, ndiye kuti
nayenso Khristu sanaukitsidwe. 17 Ndipo ngati Khristu sanaukitsidwe,
chikhulupiriro chanu n'chopanda ntchito; mukanali mu machimo anu.
18 Ndiye kuti nawonso amene agona tulo mwa Ambuye ndi otayika.
19 Ngati kukanakhala kuti tili ndi chiyembekezo mwa Khristu m'moyo uno
wokha, tikanakhala omvetsa chisoni kuposa anthu ena onse.
20 Koma n'zoonadi kuti Khristu anaukitsidwa kwa kufa, chipatso
choyamba cha onse ogona tulo. 21 Pakuti monga imfa inadza kudzera
mwa munthu, kuuka kwa akufa kwabweranso kudzera mwa munthu.
22 Pakuti monga mwa Adamu onse amafa, chomwechonso mwa Khristu
onse adzakhala ndi amoyo. 23 Koma aliyense adzauka pa nthawi yake.
Khristu ndiye woyambirira, pambuyo pake, pamene Khristu adzabwera,

iwo amene ali ake adzauka. 24 Pamenepo chimaliziro chidzafika, pamene
Iye adzapereka ufumu kwa Mulungu Atate, atathetsa ufumu wonse,
ulamuliro wonse ndi mphamvu zonse. 25 Pakuti Iye ayenera kulamulira
mpaka Mulungu atayika pansi pa mapazi ake adani ake onse. 26 Mdani
wotsiriza kuwonongedwa ndi imfa. 27 Pakuti Mulungu "wayika zinthu
zonse pansi pa mapazi ake." Ponena kuti wayika "zinthu zonse pansi pa
mapazi ake," n'chodziwikiratu kuti sakuphatikizapo ndi Mulungu yemwe,
amene anayika zinthu zonse pansi pa Khristu. 28 Pamene adzatsiriza
kuchita zimenezi, Mwana weniweniyo adzakhala pansi pa ulamuliro wa
Iye amene anayika zinthu zonse pansi pake, kuti Mulungu akhale zonse
mu zonse.

29 Tsono ngati kulibe kuuka kwa akufa, kodi iwo amene akubatizidwa
chifukwa cha akufa, adzatani? Ngati akufa saukitsidwa n'komwe,
bwanji nanga anthu akubatizidwa m'malo mwawo? 30 Ndipo kwa
ife, tikuyikiranji moyo wathu pachiswe nthawi ndi nthawi? 31 Abale,
ndimafa tsiku ndi tsiku, ndikunenetsa zimenezi, mongotsimikizira monga
ndimakunyadirani mwa Khristu Yesu Ambuye athu. 32 Ngati ndinalim-
bana ndi zirombo za kuthengo ku Efeso pa zifukwa za umunthu chabe,
ndapindulanji? Ngati akufa sadzaukitsidwa,

"Tiyeni tidye ndi kumwa,
    pakuti mawa tifa."

33 Musasocheretsedwe, "Kukhala m'magulu oyipa kumawononga
makhalidwe abwino." 34 Ganizani bwino monga kuyenerera, ndiye
lekani kuchimwa; pakuti pali ena amene sadziwa Mulungu. Ndikunena
izi kuti muchite manyazi.

### *Kuukitsidwa kwa Thupi*

35 Koma wina akhoza kufunsa kuti, "Kodi akufa amaukitsidwa motani?
Adzauka ndi thupi la mtundu wanji?" 36 Wopusa iwe! Chimene mudzala
sichikhala ndi moyo pokhapokha chitayamba chafa. 37 Mukadzala,
simudzala thupi limene lidzamere, koma mbewu chabe, mwina ya
tirigu kapena ya china chake. 38 Koma Mulungu amayipatsa thupi
monga Iye wafunira, ku mbewu ya mtundu uliwonse amapereka thupi
lakelake. 39 Mnofu siwofanana. Anthu ali ndi mnofu wa mtundu wina,
nyama zili ndi wina, mbalame zili ndi wina, nsomba zili ndi winanso.
40 Palinso matupi akumwamba ndipo palinso matupi a dziko lapansi;
koma ulemerero wa matupi akumwamba ndi wina, ndi wa matupi a
dziko lapansi ndi winanso. 41 Dzuwa lili ndi ulemerero wake, ndipo
pali ulemerero wina wa mwezi, palinso ulemerero winanso wa nyenyezi.
Ulemerero wa nyenyezi ndi wosiyanasiyana.

42 Zidzaterenso pamene akufa adzauka. Thupi loyikidwa m'nthaka
ngati mbewu limavunda, koma likadzauka lidzakhala losavunda.
43 Limayikidwa m'manda mopanda ulemu, koma likadzaukitsidwa lidza-
khala ndi ulemerero. Limayikidwa m'manda lili lofowoka, koma
likadzaukitsidwa lidzakhala ndi mphamvu. 44 Limayikidwa m'manda
thupi la mnofu chabe, koma likadzaukitsidwa lidzakhala lauzimu.

Ngati pali thupi la mnofu, palinso thupi lauzimu. 45 Kwalembedwa
kuti, "Munthu woyamba Adamu anakhala wamoyo," Adamu wotsiriza
anakhala wopatsa moyo. 46 Zauzimu sizinabwere koyambirira, koma
zachilengedwe, pambuyo pake zauzimu. 47 Munthu woyamba anali
wa dziko lapansi, wochokera m'nthaka koma munthu wachiwiri anali

wochokera kumwamba. 48 Monga analili munthu wa dziko lapansi,
momwemonso anthu onse amene ndi a dziko lapansi. Ndipo monga
alili munthu wakumwamba, momwemonso anthu onse amene ndi
akumwamba. 49 Ndipo monga momwe tinabadwa ofanana ndi munthu
wa dziko lapansi uja, momwemonso tidzakhala ofanana ndi munthu
wakumwamba.

50 Ndikunenetsa, abale, kuti thupi ndi magazi sizingathe kulowa
mu ufumu wa Mulungu, ndipo zimene zimavunda sizingathe ku-
lowa kumene zinthu sizivunda. 51 Tamverani, ndikuwuzeni chinsinsi.
Tonse sitidzagona tulo, koma tonse tidzasandulika. 52 Zidzachitika
mwadzidzidzi, m'kamphindi kochepa, monga ngati kuphethira kwa diso,
pa lipenga lotsiriza. Pakuti lipenga lidzalira, akufa adzaukitsidwa opanda
chovunda, ndipo ife tidzasandulika. 53 Pakuti chovunda chiyenera kuvala
chosavunda, ndi thupi ili lakufa liyenera kuvala losafa. 54 Pamene thupi
lovundali likadzasanduka losavunda, ndipo thupi lotha kufali likadzasan-
duka losatha kufa, pamenepo zidzakwaniritsidwa zimene zinalembedwa
zakuti, "Imfa yogonjetsedwa kwathunthu."

55 "Iwe imfa, kupambana kwako kuli kuti?
Iwe imfa, ululu wako uli kuti?"

56 Ululu wa imfa ndi tchimo, ndipo mphamvu ya tchimo ndi lamulo.
57 Koma tiyamike Mulungu amene amatipambanitsa mwa Ambuye athu
Yesu Khristu.

58 Choncho, abale anga okondedwa imani njii. Musasunthike ndi
chilichonse. Nthawi zonse mudzipereke kwathunthu ku ntchito ya
Ambuye, chifukwa mukudziwa kuti ntchito zanu mwa Ambuye sizili
zopanda phindu.

# 16

### *Ndalama Zothandizira Akhristu a ku Yerusalemu*

1 Tsopano za zopereka zothandiza anthu a Ambuye a ku Yerusalemu.
Muchite zomwe ndinawuza mipingo ya ku Galatiya kuti ichite. 2 Pa tsiku
loyamba la sabata lililonse, aliyense wa inu azipatula ndalama molin-
gana ndi zomwe wapezera. Asunge, kuti ndikabwera pasadzakhalenso
msonkhamsonkha. 3 Pamenepo, ndikadzafika, ndidzawapatsa makalata
a umboni anthu amene mudzawasankhe ndi kuwatuma kuti akapereka
mphatso zanu ku Yerusalemu. 4 Ngati kutaoneka kuti n'koyenera kuti
ndipite nawo, adzapita nane limodzi.

### *Paulo Afotokoza za Maulendo ake ndi Zina*

5 Ndidzafika kwanuko nditadutsa ku Makedoniya pakuti ndikuyem-
bekezera kudzera ku Makedoniyako. 6 Mwina ndidzakhala nanu kan-
thawi kochepa kapenanso nyengo yonse yozizira, kuti mudzandithandize
kupitiriza ulendo wanga kulikonse kumene ndingapite. 7 Sindikufuna
kuti ndikuoneni tsopano mongodutsa chabe, koma ndikuyembekezera
kudzakhala nanu kwa kanthawi, ngati Ambuye alola. 8 Koma ndikhala
ndili ku Efeso mpaka nthawi ya Pentekosite, 9 pakuti mwayi waukulu
wapezeka woti n'kugwira ntchito yaphindu, koma pali ambiri amene
akutsutsana nane.

10 Ngati Timoteyo afike kwanuko, onetsetsani kuti pasakhale zina
zomuchititsa mantha pamene ali pakati panu, pakuti iye akugwira ntchito
ya Ambuye monga ine. 11 Wina aliyense asamunyoze. Muthandizeni

kupitiriza ulendo wake mwamtendere kubwereranso kuli ine. Ndiku-
muyembekeza pamodzi ndi abale ena.
[12] Tsono kunena za m'bale wathu, Apolo, ndinamuwumiriza kwambiri
kuti abwere kwa inu abale, ndipo iye sanafune kupita tsopano. Koma
akadzapeza mpata wabwino adzabwera.
[13] Khalani tcheru; khazikikani m'chikhulupiriro chanu; limbani mtima;
khalani amphamvu. [14] Chitani zonse mwachikondi.
[15] Mukudziwa kuti a m'banja la Stefano ndiye anali oyamba kutem-
benuka mtima ku Akaya, ndipo akhala akudzipereka kutumikira oyera
mtima. Choncho ndikukudandaulirani, inu abale, [16] kuti muziwamvera
anthu oterewa, ndiponso aliyense wogwira nawo ntchitoyi modzipereka.
[17] Ndikondwera kuti Stefano, Fortunato ndi Akayiko afika, chifukwa
akhala akundithandiza pakuti inu simuli nane. [18] Pakuti anatsitsimutsa
mzimu wanga ndi wanu womwe. Anthu a mtundu oterewa ngofunika
kuwalemekeza.

### *Mawu Otsiriza*

[19] Mpingo wa m'chigawo cha ku Asiya ukupereka moni. Akula
ndi Prisila akuperekanso moni wachisangalalo, mwa Ambuye, ndiponso
mpingo umene umakumana m'nyumba mwawo ukupereka moni. [20] Abale
onse kuno akupereka moni wawo. Patsanani moni wachikondi
chenicheni.
[21] Ineyo Paulo, ndikulemba ndi dzanja langa mawu awa akuti moni.
[22] Ngati wina sakonda Ambuye akhale wotembereredwa. Maranatha!
(Ambuye athu bwerani)!
[23] Chisomo cha Ambuye Yesu chikhale ndi inu.
[24] Chikondi changa chikhale ndi nonsenu mwa Khristu Yesu.

# KALATA YACHIWIRI YA PAULO YOLEMBERA AKORINTO

1 Paulo, mtumwi wa Khristu Yesu mwachifuniro cha Mulungu, pamodzi
ndi m'bale wathu Timoteyo,

Kulembera mpingo wa Mulungu mu Korinto, pamodzi ndi oyera mtima
onse mu Akaya monse.

2 Mukhale ndi chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate
athu ndi Ambuye Yesu Khristu.

### *Mulungu Mwini Chitonthozo*

3 Alemekezeke Mulungu, Atate a Ambuye athu Yesu Khristu, Atate
achifundo chonse, Mulungu wachitonthozo chonse. 4 Iye amatitonthoza
ife m'mavuto athu onse, kuti ifenso tithe kutonthoza amene ali pavuto
lililonse ndi chitonthozo chimene ife tilandira kwa Mulungu. 5 Pakuti
monga momwe tili m'masautso pamodzi ndi Khristu, momwemonso
Khristu amatitonthoza kwambiri. 6 Ngati ife tikusautsidwa, n'chifukwa
choti inu mutonthozedwe ndi kupulumutsidwa. Ngati ife tikutonthozedwa
n'chifukwa choti inu mutonthozedwe, ndi chitonthozo chimene chimab-
weretsa mwa inu kupirira kosawiringula pa zosautsa zomwe timasauka
nazo ife. 7 Ndipo chiyembekezo chathu pa inu n'cholimba chifukwa
tikudziwa kuti monga momwe mumamva zowawa pamodzi nafe, momwe-
monso mumatonthozedwa nafe pamodzi.

8 Abale, sitikufuna kuti mukhale osadziwa za masautso amene tinaku-
mana nawo m'chigawo cha Asiya. Tinapanikizidwa koopsa kuposa
muyeso woti n'kutha kupirira, mwakuti sitinkadziwa kuti n'kukhalabe
ndi moyo. 9 Zoonadi, tinamva m'mitima mwathu chilango cha imfa.
Koma izi zimachitika kuti tisangodzidalira mwa ife tokha koma Mulungu
yemwe amaukitsa akufa. 10 Mulungu watilanditsa ku zoopsa zotere
za imfa, ndipo adzatilanditsanso. Ife tayika chiyembekezo chathu pa
Iyeyo kuti adzapitiriza kutilanditsabe. 11 Mutithandize potipempherera.
Pamenepo ambiri adzathokoza m'malo mwathu, chifukwa cha chisomo
chake poyankha mapemphero a anthu ambiri.

### *Paulo Afotokoza za Kusintha kwa Ulendo Wake*

12 Tsono chonyadira chathu n'chakuti, chikumbumtima chathu chimatit-
simikizira kuti timakhala bwino m'dziko lapansi, makamaka pa ubale
wathu ndi inu. Takhala moona mtima ndi oyera mtima. Sitinachite
chomwechi mwa nzeru ya dziko lapansi koma monga mwa chisomo
cha Mulungu. 13 Pakuti sitikukulemberani zoti simungawerenge kapena
kumvetsetsa. 14 Monga mwamva pang'ono chabe, ndikuyembekeza kuti
mudzamvetsa kwenikweni, kuti mutha kutinyadira monga ife tidzakun-
yadirani, pa tsiku la Ambuye Yesu.

15 Popeza ndinatsimikiza mtima za ichi, n'chifukwa chake ndinafuna
kuti poyamba, ndidzakuchezereni kuti mupindule pawiri. 16 Ndinafuna
kuti ndidzakuchezereni pa ulendo wanga wopita ku Makedoniya
ndi kudzakuonaninso pochokera ku Makedoniyako kuti inu mudzan-
dithandize pa ulendo wanga wopita ku Yudeya. 17 Kodi pamene
ndinkakonzekera zimenezi, mukuganiza kuti ndinkachita mwachibwana?

Kapena kuti ndinkaganiza ngati mwa dziko lapansi; kuti ndikhoza
kumanena kuti, “Inde, Inde,” nthawi yomweyo n’kumatinso “Ayi, Ayi?”
18 Koma zoona monga Mulungu ali wokhulupirika, uthenga wathu kwa
inu siwakuti, “Inde” n’kutinso “Ayi.” 19 Pakuti Yesu Khristu mwana wa
Mulungu amene ine, Silivano ndi Timoteyo tinamulalikira pakati panu
sali “Inde” yemweyonso “Ayi.” Koma nthawi zonse mwa Iye muli “Inde.”
20 Pakuti ngakhale malonjezo a Mulungu atachuluka chotani, onsewo ndi
“Inde” mwa Khristu. Kotero kuti mwa Iye, ife timati “Ameni” kuchitira
Mulungu ulemu. 21 Tsono ndi Mulungu amene anachititsa kuti inu ndi ife
tiyime molimba mwa Khristu. Anatidzoza ife, 22 nayikanso Mzimu wake
m’mitima mwathu kutitsimikizira za m’tsogolo.
23 Mulungu ndi mboni yanga kuti sindinabwererenso ku Korinto
kuno kuti ndisakumvetseni chisoni. 24 Sikuti ife tikufuna kukhala
olamulira chikhulupiriro chanu, koma timagwira nanu ntchito pamodzi
kuti mukhale achimwemwe, chifukwa ndinu okhazikika kwambiri
m’chikhulupiriro.

# 2

1 Kotero ndinatsimikiza maganizo anga kuti ndisachitenso ulendo
wina owawa wobwera kwanuko. 2 Pakuti ngati ndikumvetsani chisoni,
kodi angandisangalatse ndani, kupatula inuyo amene ndakumvetsani
chisoni? 3 N’chifukwa chake ndinakulemberani monga ndinachitiramo
kuti nditabwera kwanuko ndisadzamve chisoni ndi anthu oyenera
kundisangalatsa. Ndinali ndi chikhulupiriro ndi inu nonse kuti inuyo
mukakhala ndi chimwemwe poona kuti inenso ndili ndi chimwemwe.
4 Pakuti ndinakulemberani kalata ija ndili wopsinjika ndi wowawidwa
mtima kwambiri ndi kutuluka misozi yambiri, osati pofuna kukumvetsani
chisoni koma kuti ndikudziwitseni kuti ndimakukondani kwambiri.

### *Za Kukhululukira Wolakwa*

5 Koma ngati wina wamvetsa chisoni, sanamvetse chisoni ine ndekha,
koma koposa mosawonjezera wakhumudwitsa nonsenu, kunenatu mo-
sawonjezera. 6 Chilango chimene ambiri a inu mwamupatsa munthu
ameneyu n’chokwanira. 7 M’malo mwake tsono, muyenera kumukhulu-
lukira ndi kumulimbikitsa mtima kuti asamve chisoni choposa muyeso,
angataye mtima. 8 Choncho ndikukupemphani kuti mutsimikizire
chikondi chanu pa iye. 9 Cholinga china chimene ndinakulemberani
kalata ija chinali chofuna kukuonani ngati mudzandimvera pa zonse.
10 Aliyense amene mumukhululukire, inenso ndimukhululukira. Ndipo
ndikakhululukira, ngati pali kanthu koti ndikhululukire, ndiye kuti
ndakhululuka chifukwa cha inu pamaso pa Khristu, 11 kupewa kuti Satana
angapezere mpata pa ife, pajatu timadziwa machenjerero ake.

### *Atumiki a Pangano Latsopano*

12 Tsono nditafika ku Trowa kuti ndilalikire Uthenga Wabwino wa
Khristu, n’kupeza kuti Ambuye anditsekulira khomo, 13 ndinasowa mten-
dere mu mtima mwanga, chifukwa sindinapezeko m’bale wanga Tito.
Choncho ndinatsanzikana ndi anthu kumeneko n’kupita ku Makedoniya.
14 Koma tithokoze Mulungu amene amatitsogolera nthawi zonse monga
ogwidwa ku nkhondo a Khristu pa chipambano chake. Tsono amatig-
wiritsa ntchito yofalitsa ponseponse nzeru zodziwira Khristu ngati fungo
labwino. 15 Pakuti kwa Mulungu ndife fungo labwino la Khristu pakati

pa iwo amene akupulumutsidwa ndi amene akuwonongeka. 16 Kwa
amene akuwonongeka ndife fungo la imfa, limawapha. Ndipo kwa
amene akupulumuka ndife fungo lamoyo, limawapatsa moyo. Ndani
angayithe ntchito yotereyi? 17 Kusiyana ndi ena ambiri, ife sitilalikira
Mawu a Mulungu kuti tipeza phindu. M'malo mwake, ife mwa Khristu
timayankhula pamaso pa Mulungu moona mtima, monga anthu otumidwa
ndi Mulungu.

# 3

### *Akhristu ndi Kalata Yochokera kwa Khristu*

1 Kodi tayambanso kudzichitira umboni tokha? Kapena kodi ifenso
tikufuna makalata otivomereza kwa inu, kapena ochokera kwa inu monga
anthu ena? 2 Inu ndinu kalata yathu, yolembedwa pa mitima yathu,
yodziwika ndi yowerengedwa ndi aliyense. 3 Inu mukuonetsa kuti
ndinu kalata yochokera kwa Khristu, zotsatira za utumiki wathu, osati
yolembedwa ndi inki koma ndi Mzimu wa Mulungu wamoyo, osati pa
miyala yosemedwa koma m'mitima ya anthu.

4 Kulimba mtima kumeneku tili nako pamaso pa Mulungu kudzera
mwa Khristu. 5 Sikuti mwa ife muli kanthu kotiganizitsa kuti tingathe
kugwira ntchitoyi patokha, koma kulimba mtima kwathu kumachokera
kwa Mulungu. 6 Iye watipatsa kulimba mtima kuti tikhale atumiki a
pangano latsopano, osati malamulo olembedwa koma a Mzimu; pakuti
malamulo olembedwa amapha koma Mzimu amapereka moyo.

### *Ulemerero wa Pangano Latsopano*

7 Koma ngati utumiki umene unabweretsa imfa uja, wolembedwa
ndi malemba pa mwalawu, unabwera ndi ulemerero mwakuti Aisraeli
sanathe kuyang'anitsitsa nkhope ya Mose chifukwa cha ulemerero wa
pa nkhopeyo, ngakhale kuti unali kunka nuzilala, 8 kodi nanga utumiki
wa Mzimu sudzaposa apa? 9 Ngati utumiki umene umatsutsa anthu
unali ndi ulemerero, nanga koposa kotani ulemerero wa utumiki wob-
weretsa chilungamo! 10 Pakuti zimene zinali ndi ulemerero, tsopano
zilibenso ulemerero pofananitsa ndi ulemerero wopambanawo. 11 Ndipo
ngati zosakhalitsa zinabwera ndi ulemerero, koposa kotani ulemerero
wamuyayawo!

12 Choncho, popeza tili ndi chiyembekezo chotere, ndife olimba mtima
kwambiri. 13 Ife sitili ngati Mose amene amaphimba nkhope yake
kuopa kuti Aisraeli angaone kuti kunyezimira kwa nkhope yake ku-
mazilala. 14 Koma nzeru zawo zinawumitsidwa, pakuti mpaka lero
chophimbira chomwecho chikanalipo pamene akuwerenga Chipangano
Chakale. Sichinachotsedwebe, chifukwa chimachotsedwa ngati munthuyo
ali mwa Khristu yekha. 15 Ngakhale lero lomwe lino akuwerenga mabuku
a Mose pali chophimbabe mitima yawo. 16 Koma pamene aliyense
atembenukira kwa Ambuye, "chophimbacho chimachotsedwa." 17 Tsono
Ambuye ndi Mzimu, ndipo pamene pali Mzimu wa Ambuye, pali ufulu.
18 Ife tonse, amene ndi nkhope zosaphimba timaonetsera ulemerero wa
Ambuye, tikusinthika kufanana ndi ulemerero wake, umene ukunka
nuchulukirachulukira, wochokera kwa Ambuye, amene ndi Mzimu.

# 4

*Chuma Chosungidwa M'mbiya Zadothi*

1 Choncho popeza mwachifundo cha Mulungu tili ndi utumiki uwu,
sititaya mtima. 2 Koma ife takaniratu njira zonse zachinsinsi ndi zochititsa
manyazi. Sitichita kanthu mwachinyengo kapena mopotoza Mawu a
Mulungu. M'malo mwake, timayankhula choonadi poyera pamaso pa
Mulungu, kufuna kuti aliyense ativomereze mu mtima mwake. 3 Koma
ngakhale uthenga wathu wabwino utakhala wophimbika, ndi wophimbika
kwa okhawo amene akutayika. 4 Mulungu wa dziko lapansi anachititsa
khungu anthu osakhulupirira, kuti asathe kuona kuwala kwa Uthenga
Wabwino umene umaonetsa ulemerero wa Khristu, amene ndi chifaniziro
cha Mulungu. 5 Choncho sitilalikira za ife eni, koma Yesu Khristu monga
Ambuye, ife ndife atumiki anu chifukwa cha Yesu. 6 Pakuti Mulungu
amene anati, "Kuwala kuwunike kuchokera mu mdima," Iyeyo ndiye
anawunikira m'mitima mwathu kutipatsa kuwala kuti tidziwe ulemerero
wa Mulungu umene ukuoneka pa nkhope ya Yesu Khristu.

7 Koma tili ndi chuma ichi m'mbiya zadothi, kusonyeza kuti mphamvu
yoposayi, imachokera kwa Mulungu osati kwa ife. 8 Tapanikizika
kwambiri mbali zonse koma osaphwanyika; tathedwa nzeru koma
osataya mtima; 9 tazunzidwa, koma osasiyidwa; takanthidwa, koma
osawonongeka. 10 Nthawi zonse tikuyenda nayo imfa ya Yesu m'thupi
mwathu, kuti moyo wake Yesu uwonekenso m'thupi mwathu. 11 Pakuti
nthawi zonse, ngakhale tili ndi moyo, tikuperekedwa ku imfa chifukwa
cha Yesu, kuti moyo wake wa Yesu uwonekenso m'matupi mwathu amene
amafa. 12 Choncho imfa ikugwira ntchito mwa ife, koma moyo ukugwira
ntchito mwa inu.

13 Kwalembedwa kuti, "Ndinakhulupirira; n'chifukwa chake ndi-
nayankhula." Popeza ife tili ndi mtima womwewo wokhulupirira, ifenso
timakhulupirira ndi kuyankhula, 14 chifukwa timadziwa kuti amene
anaukitsa Ambuye Yesu kwa akufa adzatiukitsanso ife pamodzi ndi Yesu,
natipereka ife ndi inu pamaso pake. 15 Zonsezi n'kuti inu mupindule, kuti
chisomochi chifikire anthu ochuluka kwambiri, amenenso adzathokoza
mochuluka kwambiri ndi kupereka ulemerero kwa Mulungu.

16 N'chifukwa chake ife sititaya mtima. Ngakhale thupi lathu likunka
lifowokerafowokera, koma m'katimu tikulimbikitsidwa mwatsopano tsiku
ndi tsiku. 17 Pakuti masautso athu ndi opepuka ndi a kanthawi, koma
akutitengera ulemerero wamuyaya umene ndi wopambana kwambiri.
18 Motero sitiyang'ana zinthu zimene ndi zooneka ndi maso, koma zinthu
zimene ndi zosaoneka. Pakuti zimene zimaoneka ndi zosakhalitsa, koma
zimene sizioneka ndi zamuyaya.

# 5

*Matupi Atsopano*

1 Popeza tikudziwa kuti ngati msasa wa dziko lapansi umene tikukha-
lamo uwonongeka, tili ndi nyumba yochokera kwa Mulungu, nyumba
yamuyaya yakumwamba, osati yomangidwa ndi manja a anthu. 2 Pakali
pano tibuwula, ndi kulakalaka kuvala nyumba yathu ya kumwambayo,
3 chifukwa tikavala, sitidzapezekanso amaliseche. 4 Pamene tili mu
msasa uno, timalemedwa ndipo timabuwula, chifukwa sitifuna kukhala
amaliseche koma ovala nyumba yathu ya kumwamba, kuti chimene

chili chakufa chimezedwe ndi moyo. [5] Tsono ndi Mulungu amene
anatikonzeratu ife kuti tilandire zimenezi. Iye anatipatsa Mzimu ngati
chikole, kutsimikizira zimene zikubwera.
[6] N'chifukwa chake nthawi zonse timalimba mtima, ndipo timadziwa
kuti pamene tikukhala m'thupi, ndiye kuti tili kutali ndi Ambuye. [7] Ife
timakhala mwachikhulupiriro, osati mwa zooneka ndi maso. [8] Inde,
ife tikulimba mtima, ndipo tikanakonda kulekana nalo thupi lathu ndi
kukhala ndi Ambuye. [9] Choncho timayesetsa kukondweretsa Ambuye,
ngakhale tikhale m'thupi, kapena tichokemo. [10] Pakuti tonsefe tiyenera
kukaonekera pa mpando woweruza wa Khristu, kuti aliyense wa ife
akalandire zomuyenera molingana ndi zimene anachita ali m'thupi;
zabwino kapena zoyipa.

### *Ntchito Yoyanjanitsa*

[11] Tsono popeza tikudziwa tanthauzo la kuopa Ambuye, ife timayesetsa
kukopa anthu. Mulungu amatidziwa bwino lomwe, ndipo tikukhulupirira
kuti inunso mumatidziwa bwino m'mitima mwanu. [12] Sitikudzichitiranso
tokha umboni kwa inu, koma tikukupatsani mwayi oti muzitinyadira.
Tikufuna kuti muwayankhe amene amanyadira zinthu zooneka ndi maso
osati zimene zili mu mtima. [13] Ngati ndife amisala, monga amanenera
ena, n'chifukwa chofuna kuti Mulungu alemekezedwe. Ngati si ife
amisala, n'kuti inu muthandizike. [14] Pakuti chikondi cha Khristu ndicho
chimatikakamiza, chifukwa tikutsimikiza kuti mmodzi anafera anthu
onse, kotero kuti anthu onse anafanso. [15] Ndipo Iye anafera anthu onse
kuti amene ali ndi moyo, asakhale ndi moyo wofuna kudzikondweretsa
okha, koma azikondweretsa amene anawafera naukitsidwa chifukwa cha
iwowo.
[16] Choncho, kuyambira tsopano mpaka m'tsogolo ife sitiganizirapo za
munthu aliyense monga mwanzeru za umunthu, ngakhale kuti poy-
amba tinkaganiza za Khristu m'njira imeneyi, koma tsopano sititeronso.
[17] N'chifukwa chake, ngati munthu aliyense ali mwa Khristu, ndi
wolengedwa kwatsopano; zinthu zakale zapita taonani, zakhala zat-
sopano. [18] Zonsezi zichokera kwa Mulungu amene anatiyanjanitsa
ndi Iye mwini kudzera mwa Khristu ndipo anatipatsa ife utumiki wa
chiyanjanitso. [19] Mulungu ankayanjanitsa dziko lapansi kwa Iye mwini
kudzera mwa Khristu, osawerengera anthu monga mwa zochimwa zawo.
Ndipo watisungitsa ife uthenga uwu wa chiyanjanitso. [20] Choncho ife
ndi akazembe a Khristu, monga ngati Mulungu akudandaulira anthu
kudzera mwa ife. Ife tikukupemphani inu m'malo mwa Khristu kuti,
yanjanitsidwani ndi Mulungu. [21] Chifukwa cha ife, Mulungu anasandutsa
wopanda tchimoyo kukhala tchimo, kuti mwa Iye ife tikakhale chilungamo
cha Mulungu.

## 6

[1] Pogwira naye ntchito pamodzi, tikukudandaulirani kuti musan-
golandira chisomo cha Mulungu pachabe. [2] Pakuti akunena kuti,
"Pa nthawi yanga yabwino yokomera anthu mtima ndinakumvera,
ndipo pa nthawi yopulumutsa ndinakuthandiza.
Taonani, ndikukuwuzani kuti, ino ndiyo nthawi yabwino ya Ambuye, lero
ndiye tsiku la chipulumutso."

### *Masautso a Paulo*

3 Ife sitikuyika chokhumudwitsa pa njira ya wina aliyense, kuti utumiki
wathu usanyozeke. 4 M'malo mwake, mwanjira iliyonse timasonyeza
kuti ndife atumiki a Mulungu popirira kwambiri m'masautso, m'zowawa
ndi m'zodetsa nkhawa. 5 Pomenyedwa, kuponyedwa m'ndende ndi
m'zipolowe. Pogwira ntchito mwamphamvu, posagona usiku onse,
posowa chakudya; 6 pokhala moyo woyera mtima, pomvetsa zinthu,
wokoma mtima ndi wachifundo mwa Mzimu Woyera ndi mwachikondi
choonadi 7 ndi poyankhula choonadi mwamphamvu ya Mulungu.
Zida zimene zili m'dzanja lamanja ndi lamanzere ndizo chilungamo.
8 Timatumikira Mulungu ngakhale ena amatinyoza ndi ena amatile-
mekeza, ena amatinenera chipongwe, enanso amatiyamikira. Ena
amatitenga kukhala ngati onena zoona, ndipo enanso amatitenga kukhala
ngati onena zabodza. 9 Amatiyesa osadziwika komatu ndife odziwika
kwambiri. Amatiyesa wooneka ngati tikufa, koma tikupitirirabe ndi
moyo, okanthidwa, koma osaphedwa. 10 Amatiyesa achisoni, koma
ndife achimwemwe nthawi zonse, aumphawi, koma olemeretsa ambiri;
wopanda kanthu, koma tili ndi zonse.

11 Tayankhula momasuka kwa inu, Akorinto, ndipo tanena zonse za
kumtima kwathu. 12 Ife sitikukubisirani chikondi chathu pa inu, koma
inu mukubisa chikondi chanu pa ife. 13 Pofuna kufanana zochita ndi
kuyankhula monga kwa ana anga, nanunso muzinena za kukhosi kwanu.

### *Kukhala Pamodzi ndi Osakhulupirira*

14 Musamasenze goli pamodzi ndi osakhulupirira. Kodi pali mgwi-
rizano wanji pakati pa kulungama ndi kusalungama? Kapena kodi pali
mgwirizano wanji pakati pa kuwala ndi mdima? 15 Pali mgwirizano
wanji pakati pa Khristu ndi Beliyali? Kapena munthu wokhulupirira
angayanjane bwanji ndi munthu wosakhulupirira? 16 Pali mgwirizano
wanji pakati pa Nyumba ya Mulungu ndi nyumba ya mafano? Popezatu
ndife Nyumba ya Mulungu wamoyo. Monga Mulungu wanena kuti,
"Ndidzakhala mwa iwo
    ndipo ndidzayendayenda pakati pawo,
ndipo ndidzakhala Mulungu wawo,
    ndipo adzakhala anthu anga."
17 N'chifukwa chake
"Tulukani pakati pawo
    ndi kudzipatula,
        akutero Ambuye.
Musakhudze chodetsedwa chilichonse,
    ndipo ndidzakulandirani."
18 Ndipo
"Ndidzakhala Atate anu,
    ndipo inu mudzakhala ana anga aamuna ndi aakazi,
        akutero Ambuye, Wamphamvuzonse."

## 7

1 Abwenzi okondedwa, popeza tili ndi malonjezo amenewa, tiyeni
tidziyeretse, kusiyana nazo zilizonse zimene zikhoza kudetsa thupi ndi
mzimu, ndipo tiyesetse kukhala oyera mtima poopa Mulungu.

### *Chimwemwe cha Paulo*

[2] Mutipatse malo m'mitima mwanu. Ife sitinalakwire munthu aliyense,
kapena kuyipitsa munthu aliyense, kapena kumuchenjerera munthu
aliyense. [3] Sindikunena izi kuti mupezeke olakwa. Ndinanena kale
kuti ife timakuganizirani kwambiri kotero kuti tili pamodzi, ngakhale
tikhale moyo kapena timwalire. [4] Ndimakukhulupiririrani kwambiri ndipo
ndimakunyadirani kwambiri. Ndikulimbikitsidwa kwambiri; m'masautso
athu onse, chimwemwe changa chilibe malire.

[5] Pakuti titafika ku Makedoniya, sitinapume n'komwe, koma tinavutit-
sidwa mbali zonse. Kunja kunali mikangano, ndipo m'mitima mwathu
munali mantha. [6] Koma Mulungu, amene amatonthoza mtima wopsinjika,
anatitonthoza mtima ndi kufika kwa Tito, [7] sikubwera kwake kokhako,
komanso mawu achilimbikitso amene analandira kuchokera kwa inu.
Iye anatiwuza kuti mukufuna kundiona, zachisoni chanu chachikulu, ndi
kudzipereka kwanu kwa ine, motero chimwemwe changa chinachuluka
kuposa kale.

[8] Ngakhale kalata yanga ija inakupwetekani mtima, sindikudandaula
kuti ndinalemberanji. Ngakhale zinandikhudza, ndikudziwa kuti kalata
yanga inakupwetekani, koma kwa kanthawi kochepa. [9] Koma tsopano
ndine wokondwa, osati chifukwa chakuti kalatayo inakupwetekani, koma
chifukwa chakuti chisoni chanu chinakuthandizani kutembenuka mtima.
Pakuti munamva chisoni monga mmene Mulungu amafunira, choncho
simunapwetekedwe mwanjira iliyonse. [10] Chisoni chimene Mulungu
amafuna chimabweretsa kutembenuka mtima komwe kumabweretsa
chipulumutso, ndipo sichikhumudwitsa. Koma chisoni cha dziko lapansi
chimabweretsa imfa. [11] Taonani zimene chisoni chimene Mulungu ama-
funa chatulutsa mwa inu. Chatulutsa khama lalikulu, chakuthandizani
kuti mudzikonze nokha, chakukwiyitsani kwambiri, komanso chaku-
patsani mantha aakulu. Chakuchititsani kuti mufune kundiona ine,
mwakhudzidwa kwambiri ndipo mukufuna kuonetsetsa kuti chilungamo
chachitikadi. Pa nkhani yonseyi, mwaonetsadi kuti ndinu osalakwa.
[12] Choncho ngakhale ndinakulemberani kalata ija, sindinayilembe ndi
chifukwa cha amene analakwayo kapena wolakwiridwa, koma ndinay-
ilemba kuti inuyo muone kudzipereka kwanu kwa ife pamaso a Mulungu.
[13] Zimenezi zatilimbikitsa kwambiri.

Kuwonjezera pa zotilimbikitsazo, tinakondwa kwambiri poona chisan-
galalo cha Tito, chifukwa nonsenu munamuthandiza kukhazikitsa mtima
wake pansi. [14] Ndinamuwuza kuti ndimakunyadirani, ndipo simunandi-
chititse manyazi. Koma monga zonse zimene tinakuwuzani zinali zoona,
tsono zomwe ndinawuza Tito zokunyadirani zinali zoona. [15] Ndipo
chikondi chake pa inu n'chachikulu kwambiri akakumbukira kuti nonse
munali omvera, munamulandira ndi mantha ndi kunjenjemera. [16] Ndine
wokondwa kuti ndingathe kukukhulupiririrani pa zonse.

# 8

*Kulimbikitsa Zopereka*

[1] Ndipo tsopano, abale, tikufuna kuti mudziwe za chisomo chimene
Mulungu wapereka ku mipingo ya ku Makedoniya. [2] Pakati pa mayesero
owawitsa, chimwemwe chawo chosefukira ndi umphawi wawo otheratu,
anapereka mowolowamanja kwambiri. [3] Motero ndikuchitira umboni
kuti anapereka mmene akanathera, ndipo mwinanso kuposera mmene

akathera kupereka. Anapereka mosakakamizidwa, [4] ndipo anatipempha
motiwumiriza kuti tiwapatse mwayi woti nawonso athandize anthu oyera
mtima a ku Yudeya. [5] Iwo anachita moposera mmene ife timayembekez-
era. Choyamba anadzipereka kwa Ambuye ndipo kenaka kwa ife monga
mwa chifuniro cha Mulungu. [6] Choncho tinamupempha Tito kuti atsirize
poti n'kuti atayamba kale ntchito yachisomoyi pakati panu. [7] Popeza
pa zinthu zonse munachita bwino, monga pachikhulupiriro, poyankhula,
pachidziwitso, pakhama lambiri ndi pachikondi chanu pa ife, onetsetsani
kuti muchitenso bwino pachisomo ichi chopereka.

[8] Sindikukulamulirani, koma ndikufuna kuona ngati chikondi chanu
n'choona pofananitsa ndi changu cha anthu ena. [9] Pakuti mukudziwa
chisomo cha Ambuye athu Yesu Khristu, kuti ngakhale anali wolemera,
koma chifukwa cha inuyo anasanduka wosauka, kuti umphawi wakewo,
inuyo mulemere.

[10] Ndipo nawa malangizo anga pa zoyenera inu kuchita pa nkhaniyi.
Chaka chatha munali oyamba, osati ongofuna kupereka kokha komanso
okhala ndi mtima ofuna kupereka. [11] Tsopano tsirizani ntchitoyi, ndipo
changu chanu chofunitsitsa kugwira ntchitoyi ndi kuyitsiriza chichitike
molingana ndi zimene muli nazo. [12] Ndipo ngati mtima ofunitsitsa ulipo,
mphatsoyo imalandiridwa molingana ndi zimene munthuyo ali nazo, osati
zimene alibe.

[13] Cholinga chathu sikuti tipeputse ena pamene inuyo mukuvutika,
koma kuti pakhale kufanana. [14] Zambiri zimene muli nazo pakati panu
muthandize nazo osowa, kuti nawonso akadzakhala nazo zambiri adza-
kuthandizeni pa zosowa zanu. Cholinga n'kuchita mofanana, [15] monga
kwalembedwa kuti, "Iye amene anatola zambiri sizinamutsalireko ndipo
amene anatola pang'ono sizinamuchepere."

### *Tito Atumidwa ku Korinto*

[16] Tithokoze Mulungu amene anayika mu mtima wa Tito changu
chomwecho chimene ine ndili nacho pa inu. [17] Pakuti Tito sanangovomera
kokha pempho lathu, koma yekha anafunitsitsa kwambiri kubwera kwa
inu mwa iye yekha. [18] Ndipo tikumutumiza pamodzi ndi m'bale amene
mipingo yonse yamuyamikira chifukwa cha utumiki wake wa Uthenga
Wabwino. [19] Chowonjezera china n'chakuti anasankhidwa ndi mipingo
kuti atiperekeze pamene ife tikukapereka zopereka, zimene tikuchita
pofuna kupereka ulemu kwa Ambuye mwini ndi kuonetsa kufunitsitsa
kwathu pothandiza. [20] Tikufuna kupewa kutikayikira kulikonse za
mmene tikuyendetsera mphatso zochulukazi. [21] Pakuti tikuyesetsa kuchita
zolondola, osati pamaso pa Ambuye pokha komanso pamaso pa anthu.

[22] Kuwonjezera apo, tikuwatumiza pamodzi ndi m'bale wathu, amene
nthawi zambiri watitsimikizira m'njira zosiyanasiyana kuti ndi wachangu
ndiponso chifukwa ali ndi chikhulupiriro chachikulu mwa inu. [23] Kunena
za Tito, ndiye mnzanga ndi wogwira naye ntchito pakati panu. Kunena za
abale athu, ndiwo oyimirira mipingo ndi olemekezetsa Khristu. [24] Choncho
anthu amenewa atsimikizireni za chikondi chanu ndipo adziwe chifukwa
chimene ife timakunyadirani, kuti mipingo yonse iwone chimenechi.

## 9

[1] N'kosafunika kuti ndikulembereni za utumiki othandiza anthu a
Mulungu. [2] Popeza ndikudziwa mtima wanu wofuna kuthandiza, ndipo

ndakhala ndikuwawuza monyadira a ku Makedoniya za chimenechi.
Ndimawawuza kuti inu a ku Akaya munakonzeka kale chaka chatha kuti
mupereke. Ndipo changu chanu chapatsa chidwi ambiri mwa iwo kuti
nawonso achitepo kanthu. 3 Koma ndikutumiza abalewo kuti kukunyadi-
rani kwathu pa zimenezi kutsimikizike kuti si kwachabe ndi kuti mukhale
okonzeka monga ndinanenera. 4 Pakuti nditabwera kumeneko ndi abale
ena a ku Makedoniya, ndikukupezani kuti simunakonzeke, tingadzachite
manyazi chifukwa chokudalirani. Koma amene angadzachite manyazi
kwambiri ndi inuyo. 5 Choncho ndinaganiza kuti n'kofunika kupem-
pha abale kuti adzakuchezereni ineyo ndisanafike, ndikuti adzatsirize
kukonzekera mphatso zomwe munalonjeza kupereka mowolowamanja.
Motero mphatsoyo idzakhala yokonzeratu, ndipo idzakhala mphatso
yoperekedwa mowolowamanja, osati mokakamizidwa.

### *Kupereka Mowolowamanja*

6 Takumbukirani mawu awa: Amene adzala pang'ono, adzakololanso
pang'ono, ndipo amene adzala zochuluka, adzakololanso zochuluka.
7 Munthu aliyense apereke chimene watsimikiza mu mtima mwake
kuti apereka, osati monyinyirika kapena mokakamizidwa, pakuti Mu-
lungu amakonda wopereka mokondwera. 8 Ndipo Mulungu akhoza
kukudalitsani kwambiri, kuti inuyo nthawi zonse mukhale ndi zinthu
zokukwanirani, ndiponso ndi zina zochuluka kuti muthandize pa ntchito
zonse zabwino. 9 Paja analemba kuti,

"Wopereka mphatso zake mowolowamanja kwa osauka,
chilungamo chake chimanka mpaka muyaya."

10 Tsono Mulungu amene amapereka mbewu kwa wofesa, ndiponso
chakudya kuti adye, adzaperekanso mbewu m'nkhokwe zanu ndi
kuzichulukitsa. Iye adzachulukitsanso zipatso za chilungamo chanu.
11 Adzakulemeretsani pa zonse kuti mukhale owolowamanja pa nthawi
zonse. Ndipo kuwolowamanja kwanu kudzera mwa ife, kudzakhala
kuthokoza kwa Mulungu.

12 Ntchito imene mukugwirayi siyongothandiza kokha anthu a Mulungu
kupeza zosowa, komanso ikuthandiza kuti anthu ambiri ayamike Mu-
lungu. 13 Chifukwa cha ntchito imene mwawatsimikizira nokha, anthu
ena onse adzayamika Mulungu chifukwa cha kumvera kwanu kumene
kumaonekera pamene mukuvomereza Uthenga Wabwino wa Khristu,
ndiponso chifukwa chowagawira mowolowamanja iwowo pamodzi ndi
wina aliyense. 14 Ndipo iwowo adzakupempehererani mwachikondi chi-
fukwa cha chisomo choposa chimene Ambuye wakupatsani. 15 Tiyamike
Mulungu chifukwa cha mphatso zake zosaneneka!

## 10

### *Paulo Ateteza Utumiki Wake*

1 Mwa kufatsa ndi kuleza mtima kwa Khristu, ndikukupemphani,
ine Paulo amene anthu ena amati ndimachita manyazi tikaonana
maso ndi maso ndi inu, koma wosaopa pamene ndili kutali nanu!
2 Ndikukupemphani kuti ndikadzafika kumeneko ndisadzachite
kuyankhula mwamphamvu monga mmene ndimayembekezera
kudzachita kwa anthu ena amene amaganiza kuti machitidwe athu
ndi ofanana ndi anthu a dziko lapansi. 3 Ngakhale ife timakhala
m'dziko lapansi, sitimenya nkhondo monga mmene dziko lapansi

limachitira. [4] Pakuti zida zathu zankhondo si zida za dziko lapansi.
Koma ndi mphamvu zochokera kwa Mulungu zotha kugwetsa malinga.
[5] Timagonjetsa maganizo onse onyenga ndiponso kudzikuza kulikonse
kolimbana ndi anthu kuti asadziwe Mulungu. Ndipo timagonjetsa ganizo
lililonse kuti limvere Khristu. [6] Ndipo ife tidzakhala okonzeka kulanga
aliyense wosamvera ngati inuyo mutakhala omvera kwenikweni.

[7] Inu mukuweruza potengera zimene maso anu akuona. Ngati wina
akutsimikiza kuti ndi wake wa Khristu, iye aganizenso kuti ifenso ndife
a Khristu monga iye. [8] Tsono ngakhale nditadzitama momasuka za
ulamuliro umene Ambuye anatipatsa woti tikukuzeni osati kukuwonon-
gani, ndithu sindidzachita manyazi. [9] Ine sindikufuna kuoneka ngati
ndikukuopsezani ndi makalata anga. [10] Pakuti ena amati, "Makalata
ake ndi awukali ndi amphamvu koma maonekedwe a thupi lake ndi
wosagwira mtima ndipo mayankhulidwe ake ndi achabechabe." [11] Anthu
oterewa ayenera kuzindikira kuti zomwe timalemba m'makalata tili kutali
ndi zomwe tidzakhale tili komweko.

[12] Sitikudziyika kapena kudzifananiza tokha ndi anthu ena amene
amadziyenereza okha. Pamene akudzifanizira okha podziyerekeza ndi
anzawo a m'gulu lawo lomwe, ndi opanda nzeru. [13] Komabe, ifeyo
sitidzitama modutsa malire ake enieni, koma kudzitama kwathu kudza-
lekeza m'malire amene Mulungu anatiyikira, malire ake ndi mpaka kwa
inu. [14] Pakuti sitikudzitama modutsa malire ngati kuti sitinafike kwa inu,
popeza tinali oyamba kufika kwa inu ndi Uthenga Wabwino wa Khristu.
[15] Choncho sitinyadiranso ntchito imene ena anayigwira. Chiyembekezo
chathu n'chakuti, pamene chikhulupiriro chanu chikukulirakulira, dera
lathu la ntchito pakati panu lidzakulanso kwambiri, [16] kuti tikalalikire
Uthenga Wabwino mu zigawo zina kupitirira kwanuko. Pakuti sitikufuna
kudzitama pa ntchito yogwira ena kale m'dera la munthu wina. [17] Koma,
"Ngati munthu akufuna kunyadira, anyadire mwa Ambuye." [18] Pakuti
munthu amene amavomerezedwa, si amene amadziyenereza yekha, koma
munthu amene Ambuye amuyenereza.

# 11

*Paulo ndi Atumwi Onyenga*

[1] Ndikukhulupirira kuti mupirira nako pang'ono kupusa kwanga.
Chonde tandipiririrani! [2] Nsanje imene ndimakuchitirani ndi yofanana ndi
ya Mulungu. Ndinakulonjezani mwamuna mmodzi yekha, mwamunayo
ndiye Khristu, kuti ndidzakuperekeni inuyo kwa Iyeyo monga namwali
wangwiro. [3] Koma ndikuopa kuti monga Hava ananyengedwa ndi kuchen-
jera kwa njoka, mitima yanunso ingasocheretsedwe kuleka n'kudzipereka
moona mtima ndi modzipereka kwenikweni kwa Khristu. [4] Pakuti ngati
wina abwera kwa inu nalalikira Yesu wina wosiyana ndi Yesu amene
tinamulalikira, kapena ngati mulandira mzimu wina wosiyana ndi Mzimu
amene munalandira, kapena uthenga wabwino wina wosiyana ndi umene
munawuvomereza, inuyo mumangolandira mosavuta.

[5] Komatu sindikuganiza kuti ndine wotsika kwambiri kwa "atumwi
apamwamba." [6] Mwina ndikhoza kukhala wosaphunzitsidwa
kayankhulidwe, koma ndili ndi chidziwitso. Izi tinakufotokozerani
momveka bwinobwino. [7] Kodi linali tchimo kwa ine kudzichepetsa
n'cholinga chakuti ndikukwezeni pamene ndinkalalikira Uthenga

Wabwino wa Mulungu kwa inu mwaulere? [8] Ndinkalanda mipingo
ina pomalandira thandizo kwa iwo kuti ndikutumikireni. [9] Ndipo pamene
ndinali pakati panu, nditasowa kanthu, sindinalemetse munthu aliyense,
pakuti abale ena amene anachokera ku Makedoniya anandipatsa zonse
zimene ndinkazisowa. Ndayesetsa kuti ndisakhale cholemetsa kwa inu
m'njira ina iliyonse, ndipo ndidzapitiriza kutero. [10] Kunena moona
mtima molingana ndi chilungamo cha Khristu chimene chili mwa ine,
palibe amene angandiletse kudzitamandira m'zigawo za ku Akaya.
[11] N'chifukwa chiyani ndikutero? Kodi n'chifukwa choti sindikukondani?
Mulungu akudziwa kuti ndimakukondani!

[12] Ndipo ndipitiriza kuchita zomwe ndikuchitazi n'cholinga chakuti
ndisapereke mpata kwa amene akufuna kupezera mwayi woti afanane
nafe pa zinthu zimene iwowo amadzitamandira. [13] Pakuti anthu oterewa
ndi atumwi onama, antchito achinyengo, odzizimbayitsa ngati atumwi
a Khristu. [14] Sizododometsa zimenezi, pakuti Satana mwini amadziz-
imbayitsa kuoneka ngati mngelo wowunikira anthu. [15] N'zosadabwitsa
tsono ngati atumiki ake akudzizimbayitsa ngati otumikira chilungamo.
Matsiriziro awo adzalandira zoyenerana ndi ntchito zawo.

### *Paulo Anyadira Mazunzo Ake*

[16] Ndibwereze kunena kuti, wina aliyense asandiyese chitsiru. Koma
ngati mutero, mundilandire monga mmene mukhoza kulandirira chitsiru,
kuti ndinyadirepo pang'ono. [17] Kudzinyadira kwangaku, sindikuyankhula
monga mmene Ambuye akufunira koma ngati chitsiru. [18] Popeza ambiri
akudzitama monga dziko lapansi limachitira, inenso ndidzitamanso. [19] Inu
mumalolera kukhala ndi zitsiru mokondwera chifukwa mumati ndinu
anzeru! [20] Kunena zoona mumangololera aliyense; amene amakusan-
dutsani akapolo, kapena amene amakudyerani masuku pamutu, kapena
amene amakupezererani, kapena amene amadzitukumula, kapena amene
amakumenyani khofi. [21] Ndikuvomera mwamanyazi kuti ife sitinali
olimba mtima kuti n'kuchita zinthu zimenezi.

Ndikuyankhula ngati chitsiru kuti chimene wina aliyense akhoza
kudzitama nacho, Inenso ndikhoza kudzitama nachonso. [22] Kodi iwo
ndi Ahebri? Inenso ndine Mhebri. Kodi iwo ndi Aisraeli? Inenso
ndine Mwisraeli. Kodi iwo ndi zidzukulu za Abrahamu? Inenso
ndine mdzukulu wa Abrahamu. [23] Kodi iwo ndi atumiki a Khristu?
Ndikuyankhula ngati wamisala. Ine ndine woposa iwowo. Ndagwira
ntchito kwambiri kupambana iwo, ndakhala ndikuyikidwa m'ndende
kawirikawiri, ndakwapulidwapo kwambiri, kawirikawiri ndinali pafupi
kufa. [24] Andikwapulapo kasanu zikoti zija za Ayuda, makumi anayi
kuchotsapo chimodzi. [25] Katatu anandimenya ndi ndodo. Kamodzi
anandigendapo miyala. Katatu sitima yathu ya panyanja inasweka, ndipo
ndinakhala usiku ndi usana ndi kuyandama pa nyanja. [26] Ndakhala
ndikuyenda maulendo ataliatali. Moyo wanga wakhala ukukumana ndi
zoopsa pa mitsinje, zoopsa za achifwamba, zoopsa zochokera kwa abale
anga Ayuda, zoopsa zochokera kwa anthu akunja. Ndinakumana ndi
zoopsa m'mizinda, m'midzi, pa nyanja, ndi pakati pa abale onyenga.
[27] Ndakhala ndikugwira ntchito molimbika ndipo kawirikawiri ndakhala
ndikuchezera usiku wonse osagona. Ndakhala ndikumva njala ndi
ludzu ndipo kawirikawiri ndakhala wopanda chakudya. Ndakhala ndi
kuzizidwa ndi wosowa zovala. [28] Kuwonjezera pa zonsezi, tsiku ndi tsiku
ndimakhala pa chipsinjo cha nkhawa ya mipingo yonse. [29] Ndani ali

wofowoka, ine wosakhala naye m'kufowoka kwakeko? Ndani amene
mnzake amuchimwitsa, ine wosavutika mu mtima?
30 Ngati n'koyenera kudzitamandira, ndidzadzitamandira pa zinthu
zimene zimaonetsa kufowoka kwanga. 31 Mulungu, Atate a Ambuye Yesu,
amene tiyenera kumutamanda nthawi zonse, akudziwa kuti sindikunama.
32 Ku Damasiko, bwanamkubwa woyimira Mfumu Areta, anayika alonda
kuzungulira mzinda wonse kuti andigwire. 33 Koma abale anandiyika
m'dengu nanditsitsira pa chipupa kudzera pa zenera la mpandawo,
motero ndinapulumuka m'manja mwake.

# 12

## *Masomphenya a Paulo ndi Minga ya M'thupi Mwake*

1 Ndiyenera kupitiriza kudzitamandira. Ngakhale palibe choti ndipin-
dule, ndipitiriza kufotokoza za masomphenya ndi mavumbulutso ochok-
era kwa Ambuye. 2 Ndikudziwa munthu mwa Khristu amene zaka
khumi ndi zinayi zapitazo anatengedwa kupita kumwamba kwachitatu.
Sindikudziwa ngati zinachitika ali m'thupi kapena ayi, zimenezo akudziwa
ndi Mulungu. 3 Ndipo ndikumudziwa munthu ameneyu. Sindikudziwa
ngati zinachitika m'thupi kapena ayi, zimenezo akudziwa ndi Mu-
lungu. 4 Munthuyu anatengedwa kupita ku paradizo. Ndipo anamva
zinthu zosatheka kuneneka, zinthu zimene munthu saloledwa kunena.
5 Ndidzatamanda za munthu ngati ameneyu, koma sindidzadzitamandira
ine mwini kupatula za kufowoka kwanga. 6 Ngakhale nditafuna kudzi-
tamandira, sindingakhale chitsiru, chifukwa ndikunena zoona. Koma
ndimapewa kuti pasapezeke munthu wondiganizira moposera chimene
ndili chifukwa cha zimene ndimachita kapena kuyankhula, 7 kapena
chifukwa cha mavumbulutso aakulu kuposa awa. Choncho, kuti ndisadzi-
tukumule, ndinayikidwa minga m'thupi langa, wamthenga wa Satana, kuti
adzindizunza. 8 Katatu konse ndinapempha Ambuye kuti andichotsere.
9 Koma anandiwuza kuti, "Chisomo changa ndi chokukwanira, pakuti
mphamvu zanga zimaoneka kwathunthu mwa munthu wofowoka." Chon-
cho ndidzadzitamandira mokondwera chifukwa cha zofowoka zanga, kuti
m'kutero mphamvu ya Khristu ikhale pa ine. 10 Tsono, chifukwa cha
Khristu, ndimakondwera pamene ndili wofowoka, pamene akundinyoza,
pamene ndikumva zowawa, ndi pamene akundizunza ndi kundisautsa.
Pakuti pamene ndili wofowoka ndiye kuti ndili wamphamvu.

## *Paulo Akhudzidwa ndi Akorinto*

11 Ndadzisandutsa wopusa, koma inu mwandichititsa zimenezi. Nd-
inu amene munayenera kundichitira umboni. Ngakhale kuti sindine
kanthu, koma sindine wochepetsetsa kwa "atumwi apamwamba" aja.
12 Ndinapirira pokuonetserani zizindikiro za mtumwi weniweni, pochita
pakati panu zizindikiro, zodabwitsa ndi ntchito zamphamvu. 13 Kodi
inu munaoneka ochepa motani ku mipingo ina, kupatula kuti sindinali
cholemetsa kwa inu? Mundikhululukire cholakwa chimenechi!
14 Ndakonzeka tsopano kudzakuyenderani kachitatu, ndipo sindidza-
khala cholemetsa kwa inu chifukwa ndikungofuna inuyo osati zinthu
zanu. Pakuti ana sasamalira makolo koma makolo ndiwo asamalira ana.
15 Motero ndidzakondwera kukupatsani zanga zonse zimene ndili nazo ndi
kudziperekanso ine mwini chifukwa cha inu. Kodi ine ndikamakukondani
kwambiri chotere, inuyo mudzandikonda pang'ono? 16 Ena mwa inu

amavomereza kuti sindinali cholemetsa. Komabe ena amaganiza kuti
ndine wochenjera, ndipo ndinakuchenjererani. [17] Kodi ndinakudyerani
masuku pamutu kudzera mwa wina aliyense amene ndinamutumiza kwa
inu? [18] Ndinamupempha Tito kuti abwere kwanuko ndipo ndinamutumiza
pamodzi ndi m'bale wathu. Kodi kapena Tito anakudyerani masuku
pamutu? Kodi iye ndi ine sitinachite zinthu mofanana ndi Mzimu mmodzi
yemweyo?

[19] Kodi mukuyesa kuti nthawi yonseyi takhala tikudzitchinjiriza tokha?
Takhala tikuyankhula pamaso pa Mulungu monga anthu amene ali mwa
Khristu; ndipo abwenzi okondedwa, chilichonse chimene timachita ndi
chofuna kukulimbikitsani. [20] Pakuti ndikuona kuti pamene ndibwera
sindidzakupezani monga mmene ndikufunira kuti muzikhalira, ndipo
simungadzandione monga mmene mukufunira kundionera. Ndikuopa
kuti pangadzakhale mkangano, nsanje, kupserana mitima, kugawikana,
ugogodi, miseche, kudzitukumula ndi chisokonezo. [21] Ndikuopa kuti
pamene ndidzabwerenso, Mulungu adzandichepetsa pamaso panu, ndipo
ndidzamva chisoni ndi ambiri amene anachimwa kale ndipo sanalape
zonyansa, zachigololo ndi zilakolako zoyipa zimene anachita.

# 13

*Mawu Otsiriza ndi Ochenjeza*

[1] Uwu ndi ulendo wachitatu ndikubwera kudzakuyenderani.
"Nkhani itsimikizike ndi umboni wa anthu awiri kapena atatu."
[2] Ndinakuchenjezani kale pamene ndinali nanu ulendo wachiwiri uja.
Tsopano ndikubwereza ndisanafike. Ndikabweranso sindidzachitira
chifundo amene anachimwa poyamba paja kapena wina aliyense
amene anachimwa, [3] popeza mufuna chitsimikizo chakuti Khristu
akuyankhula kudzera mwa ine. Iye siwofowoka pofuna kuchita
nanu koma ndi wamphamvu pakati panu. [4] Pofuna kutsimikizira,
anapachikidwa ali wofowoka koma ali ndi moyo mwamphamvu ya
Mulungu. Chomwechonso, ife ndife ofowoka mwa Iye, koma tidzakhala
ndi moyo pamodzi naye ndi mphamvu ya Mulungu, potumikira pakati
panu.

[5] Tadzisanthulani nokha kuti muone ngati muli m'chikhulupiriro;
dziyeseni nokha. Kodi simuzindikira kuti Khristu Yesu ali mwa inu,
ngati si choncho mwalephera mayesowa? [6] Ndipo ndikhulupirira kuti
mudzazindikira kuti ife sitinalephere mayesowo. [7] Tsopano tikupemphera
kwa Mulungu kuti musadzachite kanthu kena kalikonse kolakwa. Osati
chifukwa choti anthu aone kuti ife tapambana mayesowo koma kuti
mudzachite zokhoza ngakhale anthu atamationa ngati olephera. [8] Pakuti
sitingachite chilichonse chotsutsana ndi choonadi, koma chokhacho
chovomerezana ndi choonadi. [9] Ife timasangalala kuti pamene tafowoka,
inu muli amphamvu; ndipo pemphero lathu ndi lakuti mukhale angwiro.
[10] N'chifukwa chake ndimalemba zinthu zoterezi pamene ndili kutali, kuti
ndikabwera ndisadzagwiritse ntchito ulamuliro wanga mokalipa, uwu
ndi ulamuliro umene Ambuye anandipatsa kuti ndikukuzeni inu osati
kukuwononganani.

*Malonje Otsiriza*

11 Potsiriza abale, ndikuti tsalani bwino. Yesetsani kukhala angwiro,
mvetsetsani pempho langa, khalani a mtima umodzi, khalani mwamten-
dere. Ndipo Mulungu wachikondi ndi mtendere adzakhala nanu.
12 Lonjeranani ndi mpsopsono wachiyero. 13 Anthu onse a Mulungu
akupereka moni.
14 Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu, ndi chikondi cha Mulungu, ndi
chiyanjano cha Mzimu Woyera zikhale ndi inu nonse.

# KALATA YA PAULO YOLEMBERA AGALATIYA

1 Paulo mtumwi, osati wosankhidwa ndi anthu kapena kutumidwa ndi
munthu ayi, koma Yesu Khristu, ndi Mulungu Atate amene anamuukitsa
Yesuyo kwa akufa, 2 pamodzi ndi abale onse amene ali nane,
Kulembera mipingo ya ku Galatiya:
3 Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate athu ndi Ambuye
Yesu Khristu zikhale nanu. 4 Yesuyo anadzipereka yekha chifukwa cha
machimo athu kuti atipulumutse ku njira za moyo woyipa uno, molingana
ndi chifuniro cha Mulungu ndi Atate athu. 5 Ulemerero ukhale kwa
Mulunguyo mpaka muyaya. Ameni.

*Uthenga Wabwino ndi Umodzi Wokha*

6 Ine ndikudabwa kuti mukusiya mwamsangamsanga chotere Mulungu
amene anakuyitanani mwachisomo cha Khristu ndipo mwatembenuka
ndi kutsatira uthenga wina wosiyana, 7 umene si Uthenga Wabwino konse.
Pali anthu ena amene akukusokonezani komanso akufuna kupotoza
Uthenga Wabwino wa Khristu. 8 Ngakhale ife kapena mngelo wochokera
kumwamba, akalalikira Uthenga Wabwino wosiyana ndi umene tinaku-
lalikirani uja, iyeyo akhale wotembereredwa! 9 Monga tanena kale,
tsopano ndikubwereza kunenanso kuti, "Ngati wina aliyense akulalikirani
Uthenga Wabwino wosiyana ndi umene munawulandira, iyeyo akhale
wotembereredwa."
10 Kodi tsopano ndikufuna kukopa anthu kuti andivomereze, kapena
Mulungu? Kapena ndikufuna kukondweretsa anthu? Ngati ine
ndikanakhala kuti ndikufunabe kukondweretsa anthu, sindikanakhala
mtumiki wa Khristu.

*Paulo Woyitanidwa ndi Mulungu*

11 Abale, ine ndikufuna kuti mudziwe, kuti Uthenga Wabwino umene
ndinalalikira si ochokera kwa munthu ayi. 12 Ine sindinawulandire
kuchokera kwa munthu aliyense, kapena kuphunzitsidwa; koma ndinawu-
landira mwa vumbulutso lochokera kwa Khristu.
13 Pakuti inu munamva za moyo wanga wakale m'Chiyuda, mmene
ndinkazunzira mpingo wa Mulungu koopsa ndi kuyesetsa kuwuwononga.
14 Ine ndinkapambana Ayuda ambiri a msinkhu wanga pochita za
Chiyuda, ndipo ndinali wachangu koposa pa miyambo ya makolo athu.
15 Koma Mulungu, amene anandipatula ine ndisanabadwe, ndi kundiy-
itana mwachisomo chake, atakondweretsedwa 16 kuvumbulutsa Mwana
wake mwa ine, kuti ndikalalikire Khristuyo pakati pa anthu a mitundu
ina, ine sindinapemphe nzeru kwa munthu aliyense. 17 Ine sindinapite
ku Yerusalemu kukaonana ndi amene anali atumwi ine ndisanakhale
mtumwi. M'malo mwake nthawi yomweyo ndinapita ku Arabiya ndi
kubwereranso ku Damasiko.
18 Pambuyo pake, patatha zaka zitatu, ndinapita ku Yerusalemu kukao-
nana ndi Petro ndikukhala naye masiku khumi ndi asanu. 19 Ine sindinao-
nane ndi atumwi enawo koma Yakobo yekha, m'bale wa Ambuye. 20 Ine
ndikutsimikizira inu pamaso pa Mulungu kuti zimene ndikukulemberani
si zonama ayi. 21 Pambuyo pake ndinapita ku Siriya ndi ku Kilikiya.

22 Koma sindimadziwika ndi nkhope ku mipingo ya ku Yudeya imene ili
mwa Khristu. 23 Iwo anangomva mbiri yokha yakuti, “Munthu amene
poyamba anatizunza ife, tsopano akulalikira chikhulupiriro chimene iyeyo
nthawi ina anafuna kuchiwononga.” 24 Ndipo iwo anayamika Mulungu
chifukwa cha ine.

# 2

*Atumwi Alandira Paulo*

1 Kenaka, patatha zaka khumi ndi zinayi, ndinapitanso ku Yerusalemu,
nthawi iyi ndinapita ndi Barnaba. Ndinatenganso Tito kuti apite nafe.
2 Ine ndinapita chifukwa Mulungu anachita kundionetsera kuti ndipite
ndipo ndinakakumana ndi atsogoleri mu msonkhano mwamseri ndi
kuwafotokozera Uthenga Wabwino umene ndimalalikira pakati pa anthu
a mitundu ina. Ndinachita zimenezi kuti ndikhale ndi chitsimikizo kuopa
kuti mwina ndinathamanga kapena ndimathamanga liwiro pachabe.
3 Komatu ngakhale Tito, amene anali nane sanakakamizidwe kuti achite
mdulidwe, ngakhale iyeyo anali Mgriki. 4 Nkhani iyi inayambika chifukwa
abale ena achinyengo amene analowerera pakati pathu kuti adzaone za
ufulu umene tili nawo mwa Khristu Yesu ndikuti atisandutse akapolo. 5 Ife
sitinawagonjere ndi pang’ono pomwe, n’cholinga chakuti choonadi cha
Uthenga Wabwino chikhalebe ndi ife.

6 Koma kunena za aja ankaoneka ngati ofunika kwambiri, chimene
iwo anali sichisintha kanthu kwa ine; chifukwa Mulungu alibe tsankho,
iwowo sanawonjezepo kanthu pa uthenga wanga. 7 Makamaka anaona
kuti ine ndinapatsidwa ntchito yolalikira Uthenga Wabwino kwa anthu a
mitundu ina monga momwe Petro anapatsidwa ntchito yolalikira Uthenga
Wabwino kwa Ayuda. 8 Pakuti Mulungu, amene amagwira ntchito mu
utumiki wa Petro monga mtumwi kwa Ayuda, amagwiranso ntchito mu
utumiki wanga monga mtumiki kwa anthu a mitundu ina. 9 Yakobo,
Petro ndi Yohane, amene ankatengedwa ngati mizati, atazindikira chisomo
chimene chinapatsidwa kwa ine, anagwirana chanza ndi ine ndi Barnaba
kusonyeza chiyanjano chathu. Iwo anavomereza kuti ife tipite kwa anthu
a mitundu ina ndipo iwo apite kwa Ayuda. 10 Chimene iwo anapempha
ndi chakuti ife tipitirize kukumbukira osauka, chinthu chimene ine ndinali
okonzeka kuchichita.

*Paulo Adzudzula Petro*

11 Petro atafika ku Antiokeya, ine ndinamudzudzula pa gulu chifukwa
anapezeka wolakwa. 12 Pakuti asanafike anthu otumidwa ndi Yakobo,
iye ankadya pamodzi ndi anthu a mitundu ina. Koma atafika, iyeyo
anachoka pakati pa anthuwo nakakhala pa yekha chifukwa ankaopa
anthu a m’gulu la mdulidwe. 13 Ayuda enanso anamutsata pochita
zachinyengozi, kotero kuti ngakhale Barnaba anasocheretsedwa chifukwa
cha chinyengo chawocho.

14 Koma nditaona kuti iwo sankachita molingana ndi choonadi cha
Uthenga Wabwino, ndinawuza Petro pamaso pa anthu onse kuti, “Iwe
ndiwe Myuda koma ukukhala ngati munthu wa mtundu wina, osati
Myuda. Nanga n’chifukwa chiyani ukukakamiza anthu a mitundu ina kuti
akhale ngati Ayuda?

15 “Ife amene ndife Ayuda mwachibadwa, osati anthu a mitundu ina
ochimwa, 16 tikudziwa kuti munthu salungamitsidwa pochita ntchito za

lamulo koma ndi chikhulupiriro mwa Yesu Khristu. Chomwecho, ifenso
tinakhulupirira Khristu Yesu kuti tilungamitsidwe mwachikhulupiriro
mwa Khristu ndipo osati pochita ntchito za lamulo, chifukwa palibe amene
adzalungamitsidwa pochita ntchito za lamulo.
17 “Tsono ngati ife, pamene tikufuna kulungamitsidwa mwa Khristu,
zikuonekeratu poyera kuti ndifenso ochimwa, kodi zikutanthauza kuti
Khristu amalimbikitsa uchimo? Ayi. N’kosatheka! 18 Ngati ine ndi-
manganso chimene ndinachigumula, ndikuonetsa kuti ndine wophwanya
lamulo.
19 “Pakuti pamene ndinayesera kutsatira lamulo, lamulolo linandionetsa
kuti ndine wochimwa. Choncho ndinasiya kutsatira lamulo kuti ndikhale
ndi moyo kwa Mulungu. 20 Ndinapachikidwa pa mtanda pamodzi
ndi Khristu, kotero kuti sindinenso amene ndili ndi moyo, koma ndi
Khristu amene ali ndi moyo mwa ine. Moyo umene ndili nawo
tsopano m’thupi lino, ndi moyo mwachikhulupiriro mwa Mwana wa
Mulungu, amene anandikonda nadzipereka yekha chifukwa cha ine.
21 Ine sindikukankhira kumbali chisomo cha Mulungu, chifukwa ngati
chilungamo chikanapezeka pochita ntchito za lamulo, ndiye kuti Khristu
anafa pachabe.”

# 3

*Chikhulupiriro Kapena Ntchito za Lamulo*

1 Agalatiya opusa inu, anakulodzani ndani? Tinamuonetsa poyera
pamaso panu Yesu Khristu monga wopachikidwa pa mtanda. 2 Ine
ndikufuna ndiphunzire kuchokera kwa inu chinthu chimodzi ichi: Kodi
munalandira Mzimu pochita ntchito za lamulo, kapena pokhulupirira
zimene munamva? 3 Kani ndinu opusa chotere? Inu mutayamba
ndi Mzimu, kodi mukufuna kutsiriza ndi ntchito zathupi? 4 Kodi
munavutika kwambiri pachabe, ngati kunali kwachabedi? 5 Kodi Mu-
lungu amene anakupatsani Mzimu wake ndi kuchita zodabwitsa pakati
panu, amachita zimenezi chifukwa mumachita ntchito za lamulo kapena
chifukwa mumakhulupirira zimene munamva? 6 N’chimodzimodzinso
Abrahamu, “Iye anakhulupirira Mulungu, ndipo Mulungu anamutenga
kukhala wolungama.”
7 Tsono zindikirani kuti amene akhulupirira, ndi ana a Abrahamu.
8 Malemba anaonetseratu kuti Mulungu adzalungamitsa anthu a mitundu
ina mwachikhulupiriro, ndipo ananeneratu Uthenga Wabwino kwa Abra-
hamu kuti, “Mitundu yonse ya anthu idzadalitsika kudzera mwa iwe.”
9 Choncho iwo amene ali ndi chikhulupiriro ndi odalitsidwa pamodzi ndi
Abrahamu, munthu wachikhulupiriro.
10 Onse amene amadalira ntchito za lamulo ndi otembereredwa,
pakuti zalembedwa m’Buku la Malamulo kuti, “Ndi wotembereredwa
aliyense amene sachita zonse zimene zalembedwa m’Buku la Malamulo.”
11 Chodziwikiratu n’chakuti palibe amene amalungamitsidwa pamaso
pa Mulungu ndi lamulo, chifukwa, “Wolungama adzakhala ndi moyo
mwachikhulupiriro.” 12 Koma chikhulupiriro si Malamulo, chifukwa
Malemba akuti, “Munthu amene achita zinthu izi adzakhala ndi moyo
pozichita.” 13 Khristu anatiwombola ku temberero la lamulo pokhala tem-
berero m’malo mwathu, pakuti analemba kuti, “Aliyense wopachikidwa
pamtengo ndi wotembereredwa.” 14 Iye anatiwombola ife ndi cholinga
chakuti madalitso woperekedwa kwa Abrahamu abwere kwa anthu a

mitundu ina kudzera mwa Khristu Yesu, kuti ndi chikhulupiriro tilandire
lonjezo la Mzimu.

### *Lamulo ndi Lonjezo*

15 Abale, ndiloleni ndipereke chitsanzo cha zochitika m'moyo wa tsiku
ndi tsiku. Pangano likakhazikitsidwa palibe amene angachotsepo kapena
kuwonjezerapo, choncho ndi chimodzimodzi pa nkhani iyi. 16 Malonjezo
awa anaperekedwa kwa Abrahamu ndi kwa mbewu yake. Malemba
sakunena kuti, "kwa mbewu zake," kutanthauza anthu ambiri, koma,
"kwa mbewu yako," kutanthauza munthu mmodzi, amene ndi Khristu.
17 Chimene ndikutanthauza ine ndi ichi: Malamulo amene anabwera
patatha zaka 430, sangathetse pangano limene linakhazikitsidwa kale ndi
Mulungu ndi kuliwononga lonjezolo. 18 Ngati madalitso athu akudalira
ntchito za lamulo ndiye kuti madalitsowo sakupatsidwa chifukwa cha
lonjezo. Koma Mulungu mwachisomo chake anadalitsa Abrahamu
kudzera mu lonjezo.

19 Nanga tsono cholinga cha lamulo chinali chiyani? Linaperekedwa
chifukwa cha zolakwa mpaka itafika mbewu imene lonjezo limanena.
Malamulowo anaperekedwa ndi angelo kudzera mwa m'khalapakati.
20 Ngakhale zili chomwecho, m'khalapakati sayimira mbali imodzi yokha,
koma Mulungu ndi mmodzi.

21 Kodi ndiye kuti lamulo limatsutsana ndi malonjezo a Mulungu? Ayi.
N'kosatheka! Pakuti ngati tikanapatsidwa malamulo opatsa moyo ndiye
kuti mwa lamulo tikanakhala olungama. 22 Koma Malemba akunenetsa
kuti dziko lonse lili mu ulamuliro wauchimo, kuti mwachikhulupiriro
mwa Yesu Khristu, chimene chinalonjezedwa chiperekedwe kwa amene
akhulupirira.

23 Chikhulupiriro ichi chisanabwere, ife tinali m'ndende ya lamulo,
otsekeredwa mpaka pamene chikhulupiriro chikanavumbulutsidwa.
24 Choncho lamulo linayikidwa kukhala lotiyang'anira kuti lititsogolere
kwa Khristu kuti tilungamitsidwe mwachikhulupiriro. 25 Tsopano pakuti
chikhulupiriro chabwera, ife sitilinso mu ulamuliro wa lamulo.

### *Ana a Mulungu*

26 Nonse ndinu ana a Mulungu kudzera m'chikhulupiriro mwa Khristu
Yesu, 27 pakuti nonse amene munalumikizana ndi Khristu mu ubatizo
munavala Khristu. 28 Palibe Myuda kapena Mgriki, kapolo kapena mfulu,
mwamuna kapena mkazi, pakuti nonse ndinu amodzi mwa Khristu Yesu.
29 Ngati inu muli ake a Khristu, ndiye kuti ndinu mbewu ya Abrahamu,
ndi olowam'malo molingana ndi lonjezo.

## 4

1 Chimene ndikunena ndi chakuti, ngati mlowam'malo akali
wamng'ono, sasiyana ndi kapolo, ngakhale kuti chuma chonse ndi chake.
2 Mwanayo ayenera kumvera omulera ndiponso anthu oyang'anira chuma
mpaka nthawi imene abambo ake anakhazikitsa. 3 Chomwechonso, ife
pamene tinali ana, tinali akapolo a miyambo ya dziko lapansi. 4 Koma
nthawi itakwana, Mulungu anatumiza Mwana wake, wobadwa mwa
mayi, wobadwa pansi pa lamulo, 5 kudzawombola amene anali pansi pa
lamulo, kuti tilandiridwe monga ana. 6 Ndipo popeza ndinu ana, Mulungu
anatumiza Mzimu wa Mwana wake kuti alowe m'mitima mwathu, Mzimu
amene amafuwula kuti, *"Abba,* Atate." 7 Choncho sindiwenso kapolo,

koma mwana wa Mulungu. Tsono popeza ndiwe mwana wake, Mulungu wakusandutsanso mlowam'malo.

### *Nkhawa ya Paulo chifukwa cha Agalatiya*

8 Koma poyamba pamene simunkamudziwa Mulungu, munali akapolo
a zimene mwachilengedwe si milungu. 9 Koma tsopano pakuti
mukumudziwa Mulungu, kapena ndinene kuti Mulungu akukudziwani, n'chifukwa chiyani mukubwereranso ku miyambo yofowoka
ndi yomvetsa chisoni? Kodi mukufuna musandukenso akapolo?
10 Mumasunga masiku, miyezi ndi nyengo ndi zaka. 11 Ine ndikuopa kuti
mwina ntchito zanga pa inu ndinagwira pachabe.

12 Abale, ndikukudandaulirani, mukhale ngati ine, popeza ine ndinakhala ngati inu. Inu simunandilakwire. 13 Monga inu mukudziwa
ndinkakulalikirani Uthenga Wabwino ndili wofowoka. 14 Ngakhale kuti
matendawo anali ngati mayesero kwa inu, simunandinyoze kapena kunyansidwa nane. Komatu inu munandilandira ngati kuti ndinali
mngelo wa Mulungu, ngati kuti ndinali Khristu Yesu mwini. 15 Kodi
chimwemwe chanu chonse chija chili kuti? Ine nditha kuchitira umboni kuti, ngati kukanatheka, inu mukanakolowola maso anu ndi kundipatsa.
16 Kodi tsopano ine ndasanduka mdani wanu chifukwa ndakuwuzani choonadi?

17 Anthu amenewo akuchita changu kuti akukopeni, koma changu chawocho sichabwino. Chimene iwo akufuna ndi chakuti akuchotseni inu kwa ife, kuti mukachite changu powathandiza iwowo. 18 N'kwabwino kuchita changu, ngati cholingacho chili chabwino ndi kukhala otero nthawi
zonse osati pokhapo pamene ine ndili ndi inu. 19 Ana anga okondedwa,
inu amene ine ndikukumveraninso zowawa za kubereka kufikira Khristu
atawumbidwa mwa inu, 20 ine ndikanakonda ndikanakhala nanu tsopano
kuti ndisinthe mawu anga, chifukwa ndathedwa nanu nzeru.

### *Hagara ndi Sara*

21 Tandiwuzani, inu, abale amene mukufuna kukhala pansi pa lamulo,
kodi simukudziwa chimene lamulo limanena? 22 Pakuti zinalembedwa
kuti Abrahamu anali ndi ana aamuna awiri, wina mayi wake anali kapolo
ndipo wina mayi wake anali mfulu. 23 Mwana wake wobadwa mwa
kapolo anabadwa mwathupi; koma mwana wake wobadwa mwa mfulu anabadwa monga mwa lonjezo.

24 Zinthu izi zinali ngati fanizo, pakuti amayi awiriwa akuyimira mapangano awiri. Pangano limodzi ndi lochokera m'Phiri la Sinai, ndiye
Hagara, ndipo amabereka ana amene ndi akapolo. 25 Tsono Hagara,
akuyimira Phiri la Sinai ku Arabiya amene afanizidwa ndi mzinda wa Yerusalemu wa lero, chifukwa ali mu ukapolo pamodzi ndi ana ake.
26 Koma Yerusalemu wakumwamba ndiye mfulu, ndipo ndiye mayi wathu.
27 Pakuti kwalembedwa kuti,

"Sangalala, iwe mayi wosabala,
 amene sunabalepo mwana;
imba nthungululu ndi kufuwula mwachimwemwe,
 iwe amene sunamvepo ululu wa pobereka;
chifukwa mkazi wosiyidwa adzakhala ndi ana ambiri
 kuposa mkazi wokwatiwa."

28 Tsono inu abale, ndinu ana alonjezo ngati Isake. 29 Nthawi imeneyo
mwana wobadwa mwathupi anazunza mwana wobadwa mwamphamvu

za Mzimu. Zili chimodzimodzinso lero. 30 Kodi Malemba akuti chiyani?
"Muchotse kapoloyo pamodzi ndi mwana wake, chifukwa mwana wa
kapolo sadzagawana chuma ndi mwana wamfulu." 31 Chifukwa chake,
abale, ife sindife ana akapolo, koma ana a mfulu.

# 5

### *Ufulu mwa Khristu*

1 Khristu anatimasula kuti tikhale mfulu. Tsono chirimikani, ndipo
musakodwenso m'goli la ukapolo.

2 Chonde mvetsetsani! Ine Paulo, ndikukuwuzani kuti mukalola kuchita
mdulidwe, Khristu simupindula nayenso konse. 3 Ndikubwerezanso
kuwuza munthu aliyense wovomereza kuchita mdulidwe kuti ayeneranso
kutsata Malamulo onse. 4 Inu amene mukufuna kulungamitsidwa ndi
lamulo mwachotsedwa mwa Khristu; munagwa kusiyana nacho chisomo.
5 Koma mwachikhulupiriro, ife tikudikira mwachidwi kudzera mwa
Mzimu, chilungamo chimene tikuyembekeza. 6 Pakuti mwa Khristu Yesu
mdulidwe kapena kusachita mdulidwe zilibe phindu. Chinthu chokhacho
chimene chimafunika ndi chikhulupiriro chogwira ntchito mwachikondi.

7 Inu munkathamanga mpikisano wanu wabwino. Anakuletsani ndani
kuti musamverenso choonadi? 8 Kukopeka kwanu kumeneku sikuchokera
kwa Iye amene anakuyitanani. 9 "Yisiti wapang'ono amagwira ntchito mu
buledi yense." 10 Ine ndikutsimikiza mwa Ambuye kuti inu simudzasiyana
nane maganizo. Iye amene akukusokonezani adzalangidwa, kaya iyeyo
ndiye ndani. 11 Abale, ngati ine ndikulalikirabe za mdulidwe, n'chifukwa
chiyani ndikusautsidwabe? Ngati ndikanakhala kuti sindikulalikira
chipulumutso cha mtanda, palibe amene akanakhumudwa. 12 Kunena za
amene akukuvutani, ndikanakonda akanangodzithena okha!

### *Moyo mwa Mzimu Woyera*

13 Inu abale, Mulungu anakuyitanani kuti mukhale mfulu. Koma musag-
wiritse ntchito ufulu wanuwo kuchita zoyipa zachikhalidwe cha uchimo
cha thupi lanu, koma mutumikirane wina ndi mnzake mwachikondi.
14 Pakuti malamulo onse akuphatikizidwa mu lamulo ili, "Konda mnansi
wako monga iwe mwini." 15 Ngati mupitiriza kulumana ndi kukhadzu-
lana, samalani kuti mungawonongane.

16 Choncho ine ndikuti, mulole kuti Mzimu akutsogolereni ndipo
simudzachita zofuna za thupi lanu la uchimo. 17 Pakuti thupi lanu
la uchimo limalakalaka zimene ndi zotsutsana ndi Mzimu, ndi Mzimu
zimene ndi zotsutsana ndi thupi lanu la uchimo. Ziwirizi zimadana,
kotero kuti simungachite zimene mukufuna. 18 Koma ngati Mzimu
akutsogolerani, ndiye kuti simuli pansi pa lamulo.

19 Ntchito za thupi lanu la uchimo zimaonekera poyera ndi izi: dama,
zodetsa ndi kuchita zonyansa; 20 kupembedza mafano ndi ufiti; kudana,
kukangana, kupsa mtima, kudzikonda, kugawikana, mipatuko 21 ndi
nsanje, kuledzera, mchezo ndi zina zotere. Ine ndikukuchenjezani monga
ndinachita poyamba paja kuti amene amachita zimenezi sadzalandira
ufumu wa Mulungu.

22 Koma chipatso cha Mzimu Woyera ndi chikondi, chimwemwe, mten-
dere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, kukhulupirika, 23 kufatsa
ndi kudziretsa. Palibe lamulo loletsa zimenezi. 24 Amene ali ake a

Khristu Yesu anapachika pa mtanda thupi lawo la uchimo pamodzi ndi
zokhumba zawo ndi zolakalaka zawo. 25 Popeza timakhala ndi moyo mwa
Mzimu Woyera, tiyeni tiyende pamodzi ndi Mzimu Woyera. 26 Tisakhale
odzitukumula, oputana ndi ochitirana nsanje.

# 6

### *Kuchita Zabwino kwa Onse*

1 Abale, ngati munthu agwa m'tchimo lililonse, inu amene Mzimu
amakutsogolerani, mumuthandize munthuyo ndi mtima wofatsa kuti
akonzekenso. Koma mukhale maso kuti inu nomwe mungayesedwe.
2 Thandizanani kusenza zolemetsa zanu, ndipo m'njira imeneyi mudza-
kwanitsa lamulo la Khristu. 3 Ngati wina adziyesa kanthu pamene iyeyo
sali kanthu konse, akudzinamiza yekha. 4 Munthu aliyense aziyesa yekha
ntchito zake mmene zilili. Ngati zili bwino, adzatha kunyadira chifukwa
cha ntchito zake zokhazo, iyeyo asadzifanizire ndi munthu wina wake,
5 pakuti aliyense ayenera kusenza katundu wake.

6 Koma munthu amene akuphunzira mawu, agawireko mphunzitsi wake
zinthu zonse zabwino zimene iye ali nazo.

7 Musanamizidwe: n'kosatheka kupusitsa Mulungu. Munthu amakolola
zimene wafesa. 8 Pakuti amene amafesa zokondweretsa thupi lake
la uchimo, kuchokera ku khalidwe limenelo adzakolola chiwonongeko;
amene amafesa zokondweretsa Mzimu, kuchokera kwa Mzimu adzakolola
moyo wosatha. 9 Tisatope n'kuchita zabwino, pakuti pa nthawi yoyenera
tidzakolola ngati sititopa. 10 N'chifukwa chake ngati tapeza mpata,
tiyenera kuchitira zabwino anthu onse, makamaka amene ndi a banja la
okhulupirira.

### *Osati Mdulidwe koma Kulengedwa Mwatsopano*

11 Onani zilembo zazikulu zimene ine ndikulemba ndi dzanja langa.

12 Onse amene akufuna kuoneka abwino pamaso pa anthu
akukukakamizani kuti muchite mdulidwe. Akuchita izi ndi cholinga
chimodzi chokha, chakuti apewe kuzunzidwa chifukwa cha mtanda wa
Khristu. 13 Pakuti ngakhale iwowa amene anachita mdulidwe satsata
Malamulo, komabe akufuna kuti muchite mdulidwe kuti anyadire
mdulidwe wanuwo. 14 Ine sindingathe kunyadira kanthu kena koma
mtanda wa Ambuye athu Yesu Khristu, kudzera mwa mtandawo dziko
lapansi linapachikidwa kwa ine ndi ine ku dziko lapansi. 15 Pakuti kaya
mdulidwe kapena kusachita mdulidwe, sizitanthauza kanthu; chofunika
ndi kulengedwa mwatsopano. 16 Mtendere ndi chifundo zikhale kwa onse
amene amatsata chiphunzitso ichi, ndi pa Israeli wa Mulungu.

17 Pomaliza wina asandivutitse, pakuti m'thupi mwanga muli zizindikiro
za Yesu.

18 Chisomo cha Ambuye athu Yesu Khristu zikhale ndi mzimu wanu
abale. Ameni.

# KALATA YA PAULO YOLEMBERA AEFESO

1 Paulo, mtumwi wa Khristu Yesu mwachifuniro cha Mulungu.
Kulembera oyera mtima a ku Efeso, okhulupirika mwa Khristu Yesu:
2 Chisomo ndi mtendere kwa inu zochokera kwa Mulungu Atate athu
ndi Ambuye Yesu Khristu.

### *Madalitso Auzimu mwa Khristu*

3 Tiyamike Mulungu, Atate a Ambuye athu Yesu Khristu, amene anati-
patsa madalitso onse a uzimu kumwamba mwa Khristu. 4 Dziko lapansi
lisanalengedwe, Mulungu anatisankhiratu mwa Khristu kuti tikhale oyera
mtima ndi wopanda cholakwa pamaso pake. Mwa chikondi chake,
5 Iye anakonzeratu kuti ife titengedwe ngati ana mwa Yesu Khristu,
molingana ndi kukonda kwake ndi chifuniro chake. 6 Anachita zimenezi
kuti tiziyamika ulemerero wa chisomo chake, umene watipatsa kwaulere
mwa Khristu amene amamukonda. 7 Mwa Yesu Khristu, chifukwa cha
magazi ake, ife tinawomboledwa ndi kukhululukidwa machimo athu
molingana ndi kuchuluka kwa chisomo cha Mulungu 8 chimene anatipatsa
mosawumira. Mwa nzeru zonse ndi chidziwitso, 9 Iye watiwululira
chifuniro chake chimene chinali chobisika, chimene anachikonzeratu
mwa Khristu, molingana ndi kukoma mtima kwake. 10 Chimene anakonza
kuti chichitike n'chakuti, ikakwana nthawi yake asonkhanitsa pamodzi
mwa Khristu zinthu zonse za kumwamba ndi pa dziko lapansi.
11 Iye anatisankhiratu mwa Khristu, atatikonzeratu molingana ndi
machitidwe a Iye amene amachititsa zinthu zonse kuti zikwaniritse
cholinga cha chifuniro chake, 12 n'cholinga chakuti, ife amene tinali
oyamba kukhala ndi chiyembekezo mwa Khristu, tiyamike ulemerero
wake. 13 Ndipo inunso pamene munamva mawu a choonadi, Uthenga
Wabwino wa chipulumutso chanu, munayikidwanso mwa Khristu. Mu-
takhulupirira, anakusindikizani chizindikiro pokupatsani Mzimu Woyera
amene Iye analonjeza. 14 Mzimu Woyerayo ndi chikole chotsimikizira
kuti tidzalandira madalitso athu, ndipo kuti Mulungu anatiwombola
kuti tikhale anthu ake. Iye anachita zimenezi kuti timuyamike ndi
kumulemekeza.

### *Kuyamika ndi Kupemphera*

15 Choncho, kuyambira pamene ndinamva za chikhulupiriro chanu
mwa Ambuye Yesu ndi za chikondi chanu pa oyera mtima onse, 16 ine
sindilekeza kuyamika Mulungu chifukwa cha inu. Ndimakukumbukirani
m'mapemphero anga. 17 Ndimapemphera kuti Mulungu wa Ambuye athu
Yesu Khristu, Atate a ulemerero akupatseni mzimu wa nzeru ndi wa
vumbulutso, kuti mumudziwe kwenikweni. 18 Ndimapempheranso kuti
maso a mitima yanu atsekuke ndi cholinga choti mudziwe chiyembekezo
chimene Iye anakuyitanirani, chuma cha ulemerero chomwe chili mwa
anthu oyera mtima. 19 Ndiponso ndikufuna kuti mudziwe mphamvu zake
zazikulu koposa zimene zili mwa ife amene timakhulupirira. Mphamvuyi
ndi yofanana ndi mphamvu yoposa ija 20 imene inagwira ntchito pamene
Mulungu anaukitsa Khristu kwa akufa, namukhazika Iye ku dzanja
lake lamanja m'dziko la kumwamba. 21 Anamukhazika pamwamba pa

ulamuliro onse ndi mafumu, mphamvu ndi ufumu, ndiponso pamwamba
pa dzina lililonse limene angalitchule, osati nthawi ino yokha komanso
imene ikubwerayo. 22 Ndipo Mulungu anayika zinthu zonse pansi pa
mapazi ake ndi kumusankha Iyeyo kukhala mutu pa chilichonse chifukwa
cha mpingo, 23 umene ndi thupi lake, chidzalo cha Iye amene adzaza
chilichonse mu njira iliyonse.

# 2

*Amene anali Akufa Alandira Moyo*

1 Kunena za inu, kale munali akufa chifukwa cha zolakwa zanu ndi
machimo anu, 2 mmene inu munkakhalamo pamene munkatsatira njira za
dziko lapansi ndi za ulamuliro waufumu wa mlengalenga, mzimu umene
ukugwira ntchito tsopano mwa amene samvera. 3 Nthawi ina tonsefe
tinalinso ndi moyo wonga wawo, tinkachitanso zilizonse zimene matupi
ndi maganizo athu ankafuna. Mwachibadwa chathu, tinali oyenera
chilango monga anthu ena onse. 4 Koma chifukwa cha chikondi chake
chachikulu pa ife, Mulungu amene ndi olemera m'chifundo, 5 anatipanga
kukhala amoyo ndi Khristu ngakhale pamene ife tinali akufa mu zolakwa
zathu. Koma tinapulumutsidwa mwachisomo. 6 Ndipo Mulungu anatiuk-
itsa pamodzi ndi Khristu ndi kutikhazika pamodzi ndi Iye mmwamba mwa
Khristu Yesu, 7 ndi cholinga chakuti m'nthawi imene ikubwera, Iyeyo adza-
onetse chuma choposa cha chisomo chake, choonetsedwa mwa kukoma
mtima kwake kwa ife mwa Khristu Yesu. 8 Pakuti mwapulumutsidwa
mwachisomo, kudzera m'chikhulupiriro ndipo izi sizochokera mwa inu
eni, koma ndi mphatso ya Mulungu, 9 osati ndi ntchito, kuti wina aliyense
asadzitamandire. 10 Pakuti ndife ntchito ya Mulungu, olengedwa mwa
Khristu Yesu kuti tichite ntchito zabwino, zimene Mulungu anazikonzeratu
kale kuti tizichite.

*Umodzi mwa Khristu*

11 Chifukwa chake kumbukirani kuti poyamba inu amene munali anthu
a mitundu ina mwachibadwa ndipo munkatchedwa "osachita mdulidwe"
ndi amene amadzitcha okha "a mdulidwe" (zimene zinachitika m'thupi
ndi manja a anthu). 12 Kumbukirani kuti nthawi imene inu munali
wopanda Khristu, simunkawerengedwa ngati nzika za Israeli ndipo
munali alendo pa pangano la lonjezo, wopanda chiyembekezo ndi opanda
Mulungu m'dziko lapansi. 13 Koma tsopano mwa Khristu Yesu, inu amene
nthawi ina munali kutali, mwabweretsedwa pafupi kudzera m'magazi a
Khristu.

14 Pakuti Iye mwini ndiye mtendere wathu, amene anachita kuti
awiri akhale mmodzi ndipo anagumula chotchinga, khoma la udani
lotilekanitsa, 15 pothetsa m'thupi lake lamulo pamodzi ndi zolamulira zake
ndi malangizo. Cholinga chake chinali chakuti alenge mwa Iye mwini,
munthu mmodzi watsopano kuchokera kwa abwino, motero n'kupanga
mtendere, 16 ndi kuyanjanitsa onse awiriwa m'thupi lake kwa Mulungu,
kudzera pa mtanda, umene Iye anaphapo udani wawo. 17 Iye anabwera
ndipo analalikira mtendere kwa inu amene munali kutali ndi mtendere
ndiponso kwa iwonso amene anali pafupi. 18 Pakuti mwa Iye, ife tonse
titha kufika kwa Atate mwa Mzimu mmodzi.

19 Kotero kuti, inu sindinunso alendo ndi adani, koma nzika pamodzi ndi
anthu a Mulungu ndiponso a m'banja la Mulungu. 20 Ndinu okhazikika

pa maziko a atumwi ndi a aneneri, pamodzi ndi Khristu Yesu mwini
ngati mwala wa pa ngodya. [21] Mwa Iyeyo, nyumba yonse yalumikizidwa
pamodzi ndipo yakwezedwa kukhala Nyumba yoyera mwa Ambuye.
[22] Ndipo mwa Iye, inunso mukamangidwa pamodzi ndi ena onse kukhala
nyumba yokhalamo imene Mulungu amakhala mwa Mzimu wake.

# 3

*Paulo Mlaliki wa Anthu a Mitundu Ina*

[1] N'chifukwa chake ine Paulo, ndili wam'ndende wa Khristu Yesu
chifukwa cha inu anthu a mitundu ina.

[2] Ndithudi, inu munamva za ntchito yachisomo cha Mulungu imene
anandipatsa chifukwa cha inu, [3] ndicho chinsinsi chimene chinawu-
lulidwa kwa ine mwa vumbulutso, monga ndinakulemberani kale
mwachidule. [4] Pamene mukuwerenga izi, inu mudzazindikira za chidzi-
witso changa pa chinsinsi cha Khristu, [5] chimene sichinawululidwe kwa
anthu amibado ina monga momwe tsopano chawululidwa ndi Mzimu
wa Mulungu mwa atumwi oyera ndi aneneri. [6] Chinsinsicho n'chakuti,
kudzera mu Uthenga Wabwino anthu a mitundu ina ndi olowam'malo
pamodzi ndi Aisraeli, ndi ziwalo za thupi limodzi, ndi olandira nawo
pamodzi malonjezo a mwa Khristu Yesu.

[7] Mwachisomo cha Mulungu ndi mphamvu zake, ine ndinasanduka
mtumiki wa Uthenga Wabwinowu. [8] Ngakhale ndili wamng'ono kwambiri
pakati pa anthu onse a Mulungu, anandipatsa chisomo chimenechi
cholalikira kwa anthu a mitundu ina chuma chopanda malire cha Khristu.
[9] Ndinasankhidwa kuti ndifotokoze momveka bwino kwa munthu aliyense
za chinsinsi chimenechi, chinsinsi chimene kuyambira kale chinali
chobisika mwa Mulungu amene analenga zinthu zonse. [10] Cholinga chake
tsopano n'chakuti, kudzera mwa mpingo, mafumu ndi a ulamuliro onse a
kumwamba adziwe nzeru zochuluka za Mulungu. [11] Chimenechi chinali
chikonzero chamuyaya cha Mulungu, chimene chinachitika kudzera mwa
Khristu Yesu Ambuye athu. [12] Mwa Khristu ndi mwa chikhulupiriro
chathu mwa Iye, timayandikira kwa Mulungu momasuka ndi molimbika
mtima. [13] Choncho, ine ndikukupemphani kuti musakhumudwe popeza
ndikusautsidwa chifukwa cha inu pakuti masautso angawa ndi ulemerero
wanu.

*Paulo Apempherera Aefeso*

[14] N'chifukwa chake ine ndikugwada pamaso pa Atate, [15] amene
banja lililonse kumwamba ndi pa dziko lapansi limatchulidwa ndi dzina
lawo. [16] Ndikupemphera kuti kuchokera m'chuma cha ulemerero wake
alimbikitse moyo wanu wa m'kati ndi mphamvu za Mzimu wake,
[17] kuti Khristu akhazikike m'mitima mwanu mwachikhulupiriro. Ndipo
ndikukupempherani kuti muzikike ndi kukhazikika m'chikondi [18] kuti
mukhale ndi mphamvu, kuti pamodzi ndi anthu oyera mtima onse
muthe kuzindikira kupingasa, kutalika ndi kukwera komanso kuzama
kwake kwa chikondi cha Khristu. [19] Ndikukupempherani kuti mudziwe
chikondi chija cha Khristu chopitirira nzeru za anthu, kuti mudzazidwe
kwathunthu ndi moyo wa Mulungu mwini.

[20] Tsopano kwa Iye amene angathe kuchita zochuluka kuposa zimene
tingapemphe, kapena kuganiza molingana ndi mphamvu zake zimene

zikugwira ntchito mwa ife, 21 Iyeyo akhale ndi ulemu mu mpingo ndi mwa
Khristu Yesu pa mibado yonse mpaka muyaya. Ameni.

# 4

*Umodzi M'thupi la Khristu*

1 Ine monga wam'ndende chifukwa chotumikira Ambuye, ndikukulim-
bikitsani kuti mukhale moyo woyenera mayitanidwe amene munalandira.
2 Mukhale odzichepetsa kwathunthu ndi ofatsa; mukhale oleza mtima,
ololerana wina ndi mnzake mwachikondi. 3 Muyesetse kusunga umodzi
wa Mzimu; umodzi umene umatimangirira pamodzi mu mtendere. 4 Pali
thupi limodzi ndiponso Mzimu mmodzi, monganso pali chiyembekezo chi-
modzi chimene anakuyitanirani. 5 Pali Ambuye mmodzi, chikhulupiriro
chimodzi, ubatizo umodzi; 6 Mulungu mmodzi ndi Atate a onse, ndipo ali
mwa onse.

7 Koma aliyense wa ife wapatsidwa chisomo molingana ndi muyeso wa
mphatso ya Khristu. 8 N'chifukwa chake akunena kuti,
"Iye atakwera kumwamba,
anatenga chigulu cha a m'ndende
ndipo anapereka mphatso kwa anthu."
9 Kodi mawu akuti, "Iye anakwera" akutanthauza chiyani, ngati Iyeyo
sanatsikire kunsi kwa dziko lapansi? 10 Iye amene anatsika ndi yemweyo
anakwera koposa m'mayiko a kumwamba onse, ndi cholinga choti zinthu
zonse zikhale zodzaza ndi Iye. 11 Iye ndiye amene anapereka mphatso
kwa ena kuti akhale atumwi ndi ena aneneri, ena alaliki, ndi ena abusa
ndi aphunzitsi. 12 Ntchito yawo ndi kukonza oyera mtima kuti agwire
ntchito ya utumiki kuti thupi la Khristu lilimbikitsidwe. 13 Izi zidzatifikitsa
tonse ku umodzi wachikhulupiriro, kumudziwa Mwana wa Mulungu,
kukhwima msinkhu ndi kufika pa muyeso wangwiro weniweni wopezeka
mwa Khristu.

14 Motero sitidzakhalanso makanda, ogwedezekagwedezeka ndi ma-
funde, otengekatengeka ndi mphepo iliyonse ya chiphunzitso ndi kuchen-
jera kwa anthu achinyengo amene amasocheretsa anthu ndi kuchenjera
kwawo. 15 M'malo mwake, poyankhula choonadi mwachikondi, tidzakula
mu zinthu zonse ndi kukhala thupi la Khristu, amene ndi Mutu, omwe ndi
mpingo. 16 Mwa Iye thupi lonse lalumikizidwa ndi kugwirana pamodzi ndi
mitsempha yothandizira. Likukula ndi kudzilimbitsa lokha mwachikondi,
pomwe chiwalo chilichonse chikugwira ntchito yake.

*Malangizo pa Makhalidwe a Chikhristu*

17 Tsono ine ndikukuwuzani izi, ndipo ndikunenetsa mwa Ambuye, kuti
musayendenso monga amachitira anthu a mitundu ina potsata maganizo
awo opanda pake. 18 Maganizo awo ndi odetsedwa, ndi osiyanitsidwa ndi
moyo wa Mulungu chifukwa cha umbuli umene uli mwa iwo chifukwa
cha kuwuma mtima kwawo. 19 Popeza sazindikiranso kanthu kalikonse,
adzipereka okha kuti akhumbe zonyansa, kuti achite mtundu uliwonse wa
zoyipa ndi zilakolako zosatha.

20 Koma inu simunadziwe Khristu m'njira yotere. 21 Zoonadi munamva
za Iye ndipo munaphunzitsidwa mwa Iye molingana ndi choonadi
chimene chili mwa Yesu. 22 Inu munaphunzitsidwa molingana ndi
moyo wanu wakale, kuchotsa umunthu wakale, umene ukupitirira ku-
wonongeka ndi zilakolako zachinyengo; 23 kuti mukonzedwe mwatsopano

m'mitima mwanu; 24 ndi kuti muvale umunthu watsopano, wolengedwa
kuti ufanane ndi Mulungu mu chilungamo chenicheni ndi chiyero.

25 Chifukwa chake, aliyense wa inu aleke kunama ndipo ayankhule
zoona kwa m'bale wake, pakuti ife tonse ndife ziwalo za thupi limodzi.
26 Kwiyani koma musachimwe. Dzuwa lisalowe mukanali chikwiyire.
27 Musamupatse mpata Satana. 28 Iye amene wakhala akuba asabenso,
koma agwire ntchito ndi kuchita kenakake kaphindu ndi manja ake, kuti
akhale ndi kenakake kogawana ndi amene akusowa.

29 M'kamwa mwanu musatuluke mawu aliwonse onyansa, koma
okhawo amene ndi othandiza kulimbikitsa ena molingana ndi zosowa
zawo, kuti athandize amene akawamve. 30 Ndipo musamvetse chisoni
Mzimu Woyera wa Mulungu amene mwasindikizidwa naye chizindikiro
cha tsiku la kuwomboledwa. 31 Chotsani kuzondana, ukali ndi kupsa
mtima, chiwawa ndi kuyankhula zachipongwe, pamodzi ndi choyipa
chilichonse. 32 Mukomerane mtima ndi kuchitirana chifundo wina ndi
mnzake. Khululukiranani wina ndi mnzake, monga momwe Mulungu
anakukhululukirani mwa Khristu.

# 5

1 Choncho, monga ana okondedwa, tsatirani chitsanzo cha Mulungu.
2 Muzikondana monga Khristu anakonda ife nadzipereka yekha chifukwa
cha ife monga chopereka cha fungo lokoma ndi nsembe kwa Mulungu.

3 Koma pakati panu pasamveke n'pang'ono pomwe zadama, kapena
za mtundu wina uliwonse wa chodetsa, kapena za umbombo, chifukwa
izi ndi zosayenera kwa anthu oyera a Mulungu. 4 Musamatukwane,
kuyankhula zopusa kapena kunena nthabwala zopanda pake, zomwe ndi
zosayenera, koma m'malo mwake muziyamika. 5 Dziwani ichi, palibe
wadama, wochita zonyansa kapena waumbombo, munthu wotero ali ngati
wopembedza mafano, amenewa alibe malo mu ufumu wa Khristu ndi
Mulungu. 6 Musalole wina akunamizeni ndi mawu opanda pake, pakuti
chifukwa cha zinthu ngati izi mkwiyo wa Mulungu ukubwera pa amene
samvera. 7 N'chifukwa chake musamayanjane nawo anthu otere.

8 Pajatu inu nthawi ina munali mdima, koma tsopano ndinu kuwunika
mwa Ambuye. Mukhale ngati ana akuwunika 9 (pakuti pamene pali
kuwunika pamapezekaponso zabwino zonse, chilungamo ndi choonadi).
10 Inu mufufuze chimene chimakondweretsa Ambuye. 11 Musayanjane
nazo ntchito zosapindulitsa za mdima, koma m'malo mwake muzitsutse.
12 Pakuti ndi zochititsa manyazi ngakhale kutchula zomwe zimachitika
mseri. 13 Koma kuwala kumawunikira zinthu, ndipo chilichonse chi-
maonekera poyera. Choncho chilichonse choonekera poyera chimasan-
dukanso kuwala. 14 N'chifukwa chake Malemba akuti,
"Dzuka, wamtulo iwe,
uka kwa akufa,
ndipo Khristu adzakuwalira."

15 Samalani makhalidwe anu, musakhale ngati opanda nzeru koma
ngati anzeru. 16 Gwiritsani ntchito mpata uliwonse, chifukwa masiku
ano ndi oyipa. 17 Choncho musakhale opusa, koma mudziwe zimene
Ambuye akufuna kuti muchite. 18 Musaledzere ndi vinyo, chifukwa
adzawononga moyo wanu. M'malo mwake, mudzazidwe ndi Mzimu
Woyera. 19 Muziyankhulana wina ndi mnzake mawu a Masalimo, nyimbo
za Mulungu ndi nyimbo za uzimu. Muziyimbira Ambuye movomerezana

ndi mitima yanu. 20 Muziyamika Mulungu Atate nthawi zonse chifukwa
cha zonse, m'dzina la Ambuye athu Yesu Khristu.

### *Malangizo kwa Akazi ndi Amuna M'banja*

21 Gonjeranani wina ndi mnzake, kuonetsa kuopa Khristu.
22 Inu akazi, muzigonjera amuna anu, monga mumagonjera kwa
Ambuye. 23 Pakuti mwamuna ndi mutu wa mkazi monga momwe
Khristu ali mutu wa mpingo, thupi lake, limene Iyeyo ndi Mpulumutsi
wake. 24 Tsono monga mpingo umagonjera Khristu, momwemonso akazi
akuyenera kugonjera amuna awo mu zonse.
25 Inu amuna, kondani akazi anu monga momwe Khristu anakondera
mpingo nadzipereka yekha m'malo mwa mpingowo 26 kuti awupatule
ukhale oyera, atawuyeretsa powusambitsa ndi madzi omwe ndi mawu
ake. 27 Anachita zimenezi kuti awupereke mpingowo kwa Iye mwini,
mpingo wowala ndi waulemerero, wopanda banga kapena makwinya
kapena chilema chilichonse, koma oyera ndi wangwiro. 28 Momwemonso,
amuna akuyenera kukonda akazi awo monga matupi awo. Iye amene
akonda mkazi wake adzikondanso yekha. 29 Pakuti palibe amene amadana
nalo thupi lake, koma amalidyetsa ndi kulisamalira bwino, monga momwe
Khristu amachitira ndi mpingo wake 30 pakuti ndife ziwalo za thupi
lake. 31 "Pa chifukwa ichi, mwamuna adzasiya abambo ndi amayi ake
nakaphatikana ndi mkazi wake, ndipo awiriwo adzakhala thupi limodzi."
32 Ichi ndi chinsinsi chozama, koma ine ndikunena za Khristu ndi mpingo.
33 Chomwecho, aliyense mwa inu akuyenera kukonda mkazi wake monga
adzikondera iye mwini, ndipo mkazi akuyenera kulemekeza mwamuna
wake.

## 6

### *Ana ndi Makolo Awo*

1 Inu ana, mverani makolo anu mwa Ambuye, pakuti zimenezi ndi
zoyenera. 2 "Lemekeza abambo ndi amayi ako." Limeneli ndi lamulo
loyamba lokhala ndi lonjezo. 3 Ngati ulemekeza abambo ako ndi amayi
ako, "zinthu zidzakuyendera bwino ndipo udzasangalala ndi moyo wautali
pa dziko lapansi." 4 Abambo musakwiyitse ana anu; m'malo mwake,
muwalere m'chiphunzitso ndi m'chilangizo cha Ambuye.

### *Antchito ndi Mabwana Awo*

5 Inu antchito, mverani mabwana anu mwaulemu ndi mwamantha ndi
moona mtima, monga momwe mungamvere Khristu. 6 Musawamvere
pamene akukuonani kuti akukomereni mtima, koma ngati akapolo a
Khristu ochita chifuniro cha Mulungu kuchokera mu mtima mwanu.
7 Tumikirani ndi mtima wonse, ngati kuti mukutumikira Ambuye, osati
anthu. 8 Inu mukudziwa kuti Ambuye adzamupatsa munthu aliyense
mphotho chifukwa cha ntchito yake yabwino imene anagwira, kaya
munthuyo ndi kapolo kapena mfulu.
9 Ndipo inu mabwana, muziwachitiranso chimodzimodzi antchito anu.
Musamawaopseze, popeza mukudziwa kuti Mbuye wawo ndi wanunso,
nonse Mbuye wanu ali kumwamba, ndipo Iyeyo alibe tsankho.

### *Zida Zankhondo za Mulungu*

10 Potsiriza ndikuti, dzilimbitseni mwa Ambuye ndi mwa mphamvu
zake zazikulu. 11 Valani zida zonse za Mulungu kuti muthe kuyima ndi

kukana machenjerero a Satana. 12 Pakuti sitikulimbana ndi thupi ndi
magazi, koma tikulimbana ndi maufumu, maulamuliro, mphamvu za
dziko la mdima, ndi mphamvu zoyipa kwambiri zauzimu zamlengalenga.
13 Choncho valani zida zonse za Mulungu, kuti pamene tsiku loyipa
kwambiri lifika, mudzathe kuyima chilili, ndipo mutatha kuchita zonse,
mudzayimabe mwamphamvu. 14 Tsono imani mwamphamvu, mutaman-
gira choonadi ngati lamba m'chiwuno mwanu, mutavala chilungamo
ngati chitsulo chotchinjiriza pa chifuwa. 15 Valani Uthenga Wabwino
wamtendere ku mapazi anu ngati nsapato. 16 Kuwonjezera pa zonsezi,
nyamulani chishango cha chikhulupiriro, ndipo ndi chimenechi mudzatha
kuzimitsa mivi yonse yoyaka moto ya oyipayo. 17 Valani chipewa
cha chipulumutso ndi kutenga lupanga la mzimu, limene ndi Mawu a
Mulungu. 18 Ndipo mupemphere mwa Mzimu nthawi zonse, m'mitundu
yonse ya mapemphero ndi zopempha. Ndipo pozindikira izi, khalani
achangu kupempherera oyera mtima nthawi zonse.

19 Mundipempherere inenso, kuti nthawi iliyonse pamene nditsekula
pakamwa panga, andipatse mawu kuti ndiwulule zinsinsi za Uthenga
Wabwino mopanda mantha. 20 Ndine kazembe wa Uthenga Wabwinowu
ngakhale ndili womangidwa m'ndende. Pempherani kuti ndilalikire
mopanda mantha, monga ndiyenera.

### *Mawu Otsiriza*

21 Tukiko, m'bale wanga wokondedwa ndi mtumiki wokhulupirika mwa
Ambuye, adzakuwuzani zonse kuti inunso mudziwe mmene ndilili ndi
zimene ndikuchita. 22 Ine ndikumutumiza kwa inu, kuti mudziwe za moyo
wathu, ndi kuti akulimbikitseni.

23 Mtendere, chikondi pamodzi ndi chikhulupiriro kuchokera kwa Mu-
lungu Atate ndi Ambuye Yesu Khristu zikhale ndi abale onse. 24 Chisomo
kwa onse amene amakonda Ambuye athu Yesu Khristu ndi chikondi
chosatha.

# KALATA YA PAULO YOLEMBERA AFILIPI

1 Paulo ndi Timoteyo, atumiki a Khristu Yesu.
Kulembera anthu onse oyera mtima a ku Filipi amene ali mwa Khristu
Yesu, pamodzi ndi oyang'anira ndi atumiki awo.
2 Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate athu ndi Ambuye
Yesu Khristu zikhale kwa inu.

### *Kuyamika ndi Pemphero*

3 Ndimayamika Mulungu wanga nthawi zonse ndikakumbukira inu.
4 M'mapemphero anga onse opempherera inu, nthawi zonse ndimapem-
phera ndi chimwemwe 5 chifukwa mwakhala mukundithandiza po-
lalikira Uthenga Wabwino kuyambira tsiku loyamba mpaka tsopano.
6 Sindikukayika konse kuti Iye amene anayamba ntchito yabwino mwa inu
adzayipitiriza ndi kuyimaliza mpaka pa tsiku la kubweranso kwa Khristu
Yesu.
7 Kwa ine ndi bwino kuti ndiziganiza zotere za nonsenu, popeza ndi-
makukondani, ngakhale ndikhale m'ndende, kapena pamene ndikuteteza
ndi kukhazikitsa Uthenga Wabwino, inu nonse mumagawana nane
chisomo cha Mulungu. 8 Mulungu angandichitire umboni kuti ndimaku-
lakalakani ndi chikondi cha Khristu Yesu.
9 Ndipo pemphero langa ndi lakuti chikondi chanu chipitirire kukuli-
rakulira pa chidziwitso ndi kuzama m'maganizo, 10 kuti mukhoza
kuzindikira chabwino koposa zonse ndi chiti kuti muthe kukhala wopanda
chodetsa ndi wopanda chilema kufikira tsiku la Khristu. 11 Ndipo
moyo wanu udzakhala odzazidwa ndi chipatso cha chilungamo chimene
chimachokera mwa Yesu Khristu. Pakuti zimenezi zidzapereka ulemerero
ndi matamando kwa Mulungu.

### *Maunyolo a Paulo Apititsa M'tsogolo Uthenga Wabwino*

12 Tsopano abale, ndikufuna mudziwe kuti chimene chandichi-
tikira ine chathandiza kwambiri kupititsa patsogolo Uthenga Wabwino.
13 Chotsatira chake n'chakuti zadziwika bwino lomwe kwa onse amene ali
ku nyumba yaufumu kuti ine ndili m'maunyolo chifukwa cha Khristu.
14 Moti chifukwa cha maunyolo angawa, abale ambiri alimbikitsidwa
kuyankhula Mawu a Mulungu molimbika ndi mopanda mantha.
15 N'zoonadi kuti ena amalalikira Khristu chifukwa cha kaduka ndi
mikangano, koma ena chifukwa cha zolinga zabwino. 16 Olalikira ndi
zolinga zabwinowa amachita izi mwachikondi, podziwa kuti ine ndili
muno chifukwa cha kuteteza Uthenga Wabwino. 17 Ena aja amalalikira
Khristu modzikonda osati moona mtima namaganiza kuti kutero kub-
weretsa mavuto pamene ndili m'maunyolo. 18 Nanga kodi zimenezo
zili ndi ntchito? Chofunika ndi chakuti Khristu alalikidwe, kaya ndi
mwachinyengo kapena moona. Ndipo ndikukondwera chifukwa cha
chimenechi.
Ndithu, ndidzapitirira kukondwera, 19 pakuti ndikudziwa kuti chifukwa
cha mapemphero anu ndi thandizo lochokera kwa Mzimu wa Yesu Khristu,
zimene zandionekera zidzathandiza kuti ndimasulidwe. 20 Ndili ndi
chiyembekezo chonse kuti sindidzachita manyazi ndi pang'ono pomwe,
koma ndidzakhala ndi chilimbikitso chokwanira kuti monga mwa nthawi

zonse, tsopano Khristu adzakwezedwa m'thupi langa kaya ndi m'moyo
kapena mu imfa. 21 Pakuti kwa ine kukhala moyo ndi Khristu ndipo
kufa ndi phindu. 22 Ngati nditi ndipitirire kukhala ndi moyo m'thupi
ndiye kuti kwa ine ndi kugwira ntchito yopindulitsa. Kodi ndisankhe
chiyani? Sindikudziwa. 23 Ndathinidwa ndi zinthu ziwirizi: Ndikulakalaka
kunyamuka kuti ndikakhale ndi Khristu, chimene ndi chinthu chabwino
kwambiri. 24 Komanso n'kofunika kwambiri kuti ndikhalebe m'thupi
chifukwa cha inu. 25 Ndili ndi chitsimikizo, ndikudziwa kuti ndidzakhala
ndi moyo ndipo ndidzapitirira nanu kuti nonse mupite m'tsogolo ndi
kukhala ndi chimwemwe mu chikhulupiriro 26 kuti pokhala nanunso,
kudzitamandira kwanu mwa Khristu Yesu kudzasefukire chifukwa cha
ine.

### *Moyo Woyenerana ndi Uthenga Wabwino*

27 Chilichonse chimene chingachitike, chachikulu n'chakuti mukhale
moyo ofanana ndi Uthenga Wabwino wa Khristu. Tsono ngati ndingab-
were kudzakuonani kapena kumangomva za inu ndili kutali, ndidzadziwa
kuti mwayima mwamphamvu mwa Mzimu mmodzi, kulimbika pamodzi
ngati munthu mmodzi chifukwa cha chikhulupiriro cha Uthenga Wab-
wino 28 osachita mantha ndi pang'ono pomwe ndi amene akutsutsana
nanu. Ichi ndi chizindikiro kwa iwo kuti adzawonongedwa, koma inu
mudzapulumutsidwa ndi Mulungu. 29 Pakuti inu mwapatsidwa mwayi
osati ongokhulupirira Khristu kokha, koma wakumva zowawa m'malo
mwa Khristu. 30 Inunso mukudutsa m'zowawa zomwe zija munaona
ndikudutsamo inenso ndipo pano mukumva kuti ndikukumana nazobe.

## 2

### *Kutsanzira Kudzichepetsa kwa Khristu*

1 Ngati muli ndi chilimbikitso chilichonse chifukwa cholumikizana ndi
Khristu, ngati muli ndi chitonthozo chifukwa cha chikondi chake, ngati
muli ndi mtima umodzi mwa Mzimu, ndipo ngati mumakomerana mtima
ndi kuchitirana chifundo, 2 tsono tsirizani chimwemwe changa pokhala
amaganizo ofanana, achikondi chimodzimodzi, amodzi mu mzimu ndi
acholinga chimodzinso. 3 Musachite kalikonse ndi mtima odzikonda chabe
kapena odzitukumula chabe. Koma khalani odzichepetsa ndipo aliyense
aziona mnzake ngati womuposa iyeyo. 4 Musamangofuna zokomera inu
nokha koma aliyense azifuna zokomeranso ena.

5 Pa ubale wanu wina ndi mnzake, mukhale ndi mtima wofanana ndi
wa Khristu Yesu:

6 Iyeyu, pokhala Mulungu ndithu,
sanatenge kufanana ndi Mulungu kukhala chinthu choyenera kuchig-
wiritsa.
7 Koma anadzichepetsa kotheratu
nakhala ndi khalidwe ngati la kapolo
ndi kukhala munthu ngati anthu ena onse.
8 Ndipo pokhala munthu choncho
anadzichepetsa yekha
ndipo anamvera mpaka imfa yake,
imfa yake ya pamtanda!
9 Choncho Mulungu anamukweza Iye kukhala wapamwamba kwambiri,
ndipo anamupatsa dzina loposa dzina lina lililonse

10 kuti pakumva dzina la Yesu, bondo lililonse limugwadire,
kumwamba ndi pa dziko lapansi ndi pansi pa dziko,
11 ndipo lilime lililonse livomereze kuti Yesu Khristu ndi Ambuye
kuchitira ulemu Mulungu Atate.

### *Kuwala monga Nyenyezi*

12 Tsono, abwenzi anga okondedwa, monga mwakhala omvera nthawi
zonse, osati pamene ndinali nanu pokha, koma tsopano koposa pamene
ndili kutali. Pitirizani kugwira ntchito ya chipulumutso chanu mwa
mantha ndi kunjenjemera, 13 pakuti ndi Mulungu amene amagwira ntchito
mwa inu kuti mufune ndi kuchita zimene zimamukondweretsa Iyeyo.

14 Muzichita zonse mosawiringula kapena mosatsutsapo, 15 kuti mukhale
wopanda cholakwa ndi angwiro, ana a Mulungu wopanda cholakwika
mu m'bado uno wachinyengo ndi wosocheretsa. Mukatero mudzawala
pakati pawo ngati nyenyezi zakumwamba 16 powawuza mawu amoyo.
Ndipo ine ndidzatha kunyadira pa tsiku la Khristu kuti sindinathamange
kapena kugwira ntchito pachabe. 17 Koma ngakhale ndikuthiridwa ngati
nsembe ya chakumwa yoperekedwa pa nsembe ndi pa utumiki wochokera
m'chikhulupiriro chanu, ndine wokondwa ndi wosangalala pamodzi ndi
inu nonse. 18 Chomwechonso, inu khalani okondwa ndi osangalala nane
pamodzi.

### *Timoteyo ndi Epafrodito*

19 Ngati Ambuye Yesu alola, ndikukhulupirira kuti ndidzamutuma
Timoteyo msanga kwanuko, kuti mwina ndingadzasangalale ndikadzamva
za moyo wanu. 20 Ndilibenso wina monga iyeyu amene ali ndi chidwi
chenicheni pa za moyo wanu. 21 Pakuti aliyense amangofuna zokomera
iye yekha osati zokomera Yesu Khristu. 22 Koma inu mukudziwa kuti
Timoteyo wadzionetsa yekha, chifukwa watumikira ndi ine pa ntchito
ya Uthenga Wabwino monga mwana ndi abambo ake. 23 Choncho
ndikuyembekezera kumutuma msanga ndikangodziwa mmene zinthu
zanga ziyendere. 24 Ndipo ndikukhulupirira kuti Ambuye akalola ine
mwini ndidzafikanso kwanuko posachedwapa.

25 Koma ndikuganiza kuti n'kofunika kuti ndikutumizireni m'bale
wanga Epafrodito, mtumiki mnzanga ndi msilikali mnzanga, amenenso
ndi mtumiki wanu amene munamutumiza kuti adzandithandize pa
zosowa zanga. 26 Pakuti akukulakalakani nonsenu ndipo akusauka mu
mtima chifukwa munamva kuti akudwala. 27 Zoonadi ankadwala ndipo
anatsala pang'ono kumwalira. Koma Mulungu anamuchitira chifundo,
ndipo sanangomuchitira chifundo iye yekhayu komanso ine, kuti chisoni
changa chisachuluke. 28 Choncho khumbo langa lofulumiza kumutumiza
lakula, kuti pamene mumuonenso musangalale komanso kuti nkhawa
yanga ichepe. 29 Mulandireni mwa Ambuye ndi chimwemwe chachikulu,
ndipo anthu onga iyeyu muziwachitira ulemu. 30 Iyeyu anatsala pang'ono
kufa chifukwa cha ntchito ya Khristu, anayika moyo pa chiswe kuti
akwaniritse thandizo limene inu simukanatha.

## 3

### *Osakhulupirira za Thupi*

1 Abale anga, ndikupitiriza kunena kuti, kondwani mwa Am-
buye! Sizondivuta kuti ndilembenso mawu omwewo, ndipo zimenezi
n'zokuthandizani inuyo.
2 Chenjerani ndi agalu amenewa, anthu ochita zoyipa, anthu amene
amadula thupi lawo. 3 Pakuti ochita mdulidwe weniweni ndife. Ife amene
timatumikira Mulungu motsogozedwa ndi Mzimu. Ife amene timanyadira
Khristu, ndipo sitidalira zinthu za thupi 4 ngakhale kuti ineyo ndili ndi
zifukwa zokwanira kudalira zinthu za thupizo.
Ngati pali winanso amene akuganiza kuti ali ndi zifukwa zokwanira
kudalira zinthu za thupi, ineyo ndili ndi zifukwa zoposa pamenepo.
5 Ndinachita mdulidwe pa tsiku lachisanu ndi chitatu nditangobadwa.
Ndine wa mtundu wa Israeli, wa fuko la Benjamini, Mhebri wa Ahebri,
kunena za malamulo, ndinali Mfarisi. 6 Kunena za changu changa,
ndinkazunza mpingo. Kunena za chilungamo chopezeka chifukwa
chotsata malamulo, ineyo ndinali wopanda cholakwa.
7 Koma zonse zimene ndinkaziyesa zaphindu, tsopano ndikuziona
kuti n'zosapindulitsa chifukwa cha Khristu. 8 Kuwonjeza pamenepo,
ndikuziona zonse kuti n'zopanda phindu poyerekeza ndi phindu lopam-
bana la kudziwa Khristu Yesu Ambuye anga. N'chifukwa cha Yesuyo
ndataya zinthu zonse ndipo ndikuziyesa zinyalala kuti ndipindule Khristu
9 ndi kuti ndipezeke mwa Iyeyo, osati ndi chilungamo changa chobw-
era chifukwa chotsata malamulo, koma chimene chimabwera chifukwa
chokhulupirira Khristu. Chilungamochi n'chochokera kwa Mulungu,
timachilandira mwachikhulupiriro. 10 Ine ndikufuna kudziwa Khristu,
ndithu, kudziwa mphamvu zake za kuuka kwa akufa. Ndikufuna
kuyanjana naye m'masautso ake, kufanana naye pa imfa yake 11 kuti
nanenso ndidzaukitsidwe kwa akufa.

### *Kuthamanga Mpaka Kumapeto pa Mpikisano wa Liwiro*

12 Sikuti ndazipeza kale zonsezi, kapena kuti ndakhala kale wangwiro,
koma ndikuthamangabe ndi kuyesetsa kuti ndipeze chimene Khristu Yesu
anandiyitanira. 13 Abale, sindidziyesera ndekha kuti ndachipeza kale
chimenechi. Koma chinthu chimodzi chimene ndimachita, n'kuyiwala
zam'mbuyo ndi kuthamangira molimbika zinthu zimene zili m'tsogolo
mwanga. 14 Ndikuthamangira kokathera mpikisanowo kuti ndikalandire
mphotho imeneyi kumwamba, imene Mulungu anandiyitanira mwa
Khristu Yesu.

### *Kutsanzira Paulo*

15 Choncho ife tonse amene tili okhwima pa moyo wauzimu, tikhale ndi
maganizo omwewa. Ndipo ngati pena ndi pena muli ndi maganizo osiyana
ndi amenewa, pameneponso Mulungu adzakuwunikirani. 16 Tiyeni ife
tizikhala mogwirizana ndi zimene tinapeza kale basi.
17 Abale, nonsenu pamodzi mudzinditsanzira ine, ndipo monga inu muli
ndi chitsanzo, phunzirani kwa amene akukhala moyo motsatira momwe
timakhalira. 18 Pakuti monga ndakhala ndikukuwuzani kawirikawiri
m'mbuyomu, ndipo tsopano ndikunenanso ndi misozi kuti, anthu ambiri
akukhala monga adani a mtanda wa Khristu. 19 Mapeto awo ndi
chiwonongeko, mulungu wawo ndi mimba zawo, ndipo ulemerero wawo
ndi manyazi awo. Mtima wawo uli pa zinthu za dziko lapansi. 20 Koma
ife ndife nzika za kumwamba ndipo tikudikirira mwachidwi Mpulumutsi
wochokera kumeneko, Ambuye Yesu Khristu. 21 Iyeyo, ndi mphamvu

imene imamuthandiza kukhazikitsa zinthu zonse pansi pa ulamuliro
wake, adzasintha matupi athu achabewa kuti akhale ofanana ndi thupi
lake la ulemerero.

# 4

1 Tsono abale anga, ndimakukondani ndipo ndikukulakalakani. Ndinu
chimwemwe changa ndi chipewa cha ulemerero wanga. Abwenzi
okondedwa, chilimikani choncho mwa Ambuye.

2 Ndikudandaulira Euodiya ndi Suntuke kuti akhale ndi mtima umodzi
mwa Ambuye. 3 Inde, ndikupempha iwe mnzanga pa ntchitoyi, thandiza
amayiwa amene ndagwira nawo ntchito ya Uthenga Wabwino pamodzi
ndi Klementonso ndi ena onse antchito anzanga amene mayina awo ali
m'buku lamoyo.

## *Malangizo Otsiriza*

4 Nthawi zonse muzikondwa mwa Ambuye. Ndikubwerezanso;
muzikondwa! 5 Kufatsa kwanu kuzioneka pamaso pa anthu onse.
Ambuye anu ali pafupi. 6 Musade nkhawa ndi kanthu kalikonse, koma
pa china chilichonse, mwa pemphero ndi chidandaulo pamodzi ndi
chiyamiko, perekani zopempha zanu kwa Mulungu. 7 Ndipo mtendere wa
Mulungu, umene upambana nzeru zonse udzasunga bwino mitima yanu
ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu.

8 Potsiriza, abale, muziyika mtima wanu pa zinthu zilizonse zabwino
ndi zotamandika monga, zinthu zoona, zinthu zolemekezeka, zinthu zol-
ungama, zinthu zoyera, zinthu zokongola ndi zinthu zosiririka. 9 Muzichita
chilichonse chimene mwaphunzira kapena kulandira kapena kumva ku-
chokera kwa ine kapena mwaona mwa ine. Ndipo Mulungu wamtendere
adzakhala nanu.

## *Kuthokoza Chifukwa cha Mphatso*

10 Ndikukondwa kwambiri mwa Ambuye kuti patapita nthawi tsopano
mwayambanso kuonetsa kuti mumandiganizira. Zoonadi, mwakhala
mukundikumbukira, koma munalibe mpata woti muonetsere zimenezi.
11 Sindikunena izi chifukwa choti ndikusowa thandizo, poti ine ndaphun-
zira kukhala wokwaniritsidwa ndi zimene ndili nazo. 12 Ndimadziwa
kusauka n'kutani, ndipo ndimadziwa kulemera n'kutani. Ndaphunzira
chinsinsi chokhala wokhutitsidwa mwa njira ina iliyonse, kaya n'kudya
bwino kapena kukhala ndi njala, kaya kukhala ndi chuma kapena
umphawi. 13 Ndikhoza kuchita zonse kudzera mwa Iye amene amandi-
patsa mphamvu.

14 Komatu munachita bwino kundithandiza m'mavuto anga. 15 Ndipo
inu Afilipi mukudziwa kuti masiku oyambirira olalikira Uthenga Wab-
wino, nditachoka ku Makedoniya, panalibe mpingo ndi umodzi omwe
umene unagwirizana nane pa nkhani yopereka ndi kulandira, kupatula
inu. 16 Pakuti ngakhale pamene ndinali ku Tesalonika, munanditumizira
kangapo zondithandiza pa zosowa zanga. 17 Osati ndikufuna mphatso
zanu, koma ndikufuna kuti pa zimene muli nazo pawonjezerekepo
phindu. 18 Ndalandira zonse ndipo ndili nazo zokwanira zoposa zosowa
zanga popeza ndalandira kwa Epafrodito mphatso zochuluka zimene
munatumiza. Ndizo zopereka za fungo labwino, nsembe zolandiridwa
zokondweretsa Mulungu. 19 Ndipo Mulungu wanga adzakwaniritsa
zosowa zanu monga mwa chuma chake chaulemerero mwa Khristu Yesu.

[20] Kwa Mulungu ndi Atate athu, kukhale ulemerero mpaka muyaya. Ameni.

### *Malonje Otsiriza*

[21] Perekani moni kwa oyera mtima onse mwa Khristu Yesu. Abale amene
ali ndi ine akupereka moni wawo. [22] Oyera mtima onse akupereka moni,
makamaka iwo a ku nyumba ya Kaisara.
[23] Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu chikhale ndi mzimu wanu. Ameni.

# KALATA YA PAULO YOLEMBERA AKOLOSE

1 Paulo, mtumwi wa Khristu Yesu mwachifuniro cha Mulungu, ndi
Timoteyo m'bale wathu.
2 Kulembera abale oyera mtima ndi okhulupirira a ku Kolose mwa
Khristu.
Chisomo ndi mtendere kwa inu zochokera kwa Mulungu Atate athu.

*Kuyamika ndi Pemphero*

3 Timayamika Mulungu Atate wa Ambuye athu Yesu Khristu, nthawi
zonse pamene tikukupempehererani. 4 Timayamika chifukwa tinamva za
chikhulupiriro chanu mwa Khristu Yesu ndi za chikondi chanu pa oyera
mtima onse. 5 Chikhulupiriro ndi chikondi, gwero lake ndi chiyembekezo
chomwe muli nacho chodzalandira zimene anakusungirani kumwamba.
Munamva kale za zimenezi kudzera m'mawu a choonadi, Uthenga
Wabwino 6 umene unafika kwa inu. Pa dziko lonse lapansi Uthenga
Wabwino ukubereka chipatso ndi kukula monga momwe zakhala zikuchi-
tikira pakati panu kuyambira tsiku limene munawumva ndi kuzindikira
chisomo cha Mulungu mu choonadi chonse. 7 Inu munaphunzira zimenezi
kuchokera kwa Epafra, mtumiki mnzathu wokondedwa, amene ndi
mtumiki wokhulupirika wa Khristu m'malo mwathu. 8 Iye anatiwuza za
chikondi chanu chimene Mzimu anakupatsani.
9 Chifukwa cha ichi, kuyambira tsiku limene tinamva za inu, sitinasiye
kukupempehererani ndi kumupempha Mulungu kuti akudzazeni ndi
chidziwitso cha chifuniro chake kudzera mu nzeru yonse yauzimu ndi
kumvetsetsa. 10 Ndipo tikupempherera zimenezi ndi cholinga chakuti inu
mukhale moyo oyenera Ambuye ndi kumukondweretsa m'njira zonse.
Kubereka chipatso pa ntchito iliyonse yabwino, ndi kukula m'chidziwitso
cha Mulungu. 11 Timapempheranso kuti Mulungu akulimbikitseni ndi
mphamvu yake yonse ya ulemerero wake, kuti muzipirira zonse ndi
mitima yofatsa ndi ya chimwemwe 12 ndi kuyamika Atate nthawi zonse,
amene wakuyenerezani kuti mulandire nawo chuma cha oyera mtima
mu ufumu wa kuwunika. 13 Pakuti Iye anatipulumutsa ku ulamuliro
wa mdima ndi kutibweretsa mu ufumu wa Mwana wake wokondedwa.
14 Mwa Iyeyu ife tinawomboledwa ndi kukhululukidwa machimo.

*Kupambana Koposa kwa Khristu*

15 Mwanayu ndiye chithunzi cha Mulungu wosaonekayo. Iye ndiye
Mwana wake woyamba kubadwa ndi wolamulira zolengedwa zonse.
16 Pakuti zinthu zonse zinalengedwa kudzera mwa Iye. Zinthu za-
kumwamba ndi za pa dziko lapansi, zooneka ndi zosaoneka, maufumu,
akuluakulu, aulamuliro ndi amphamvu. Zinthu zonse zinalengedwa
kudzera mwa Iye ndipo anazilengera Iyeyo. 17 Iyeyo analipo zinthu
zonse zisanalengedwe ndipo zinthu zonse zimamangika pamodzi mwa Iye.
18 Iye ndiyenso mutu wa thupi, limene ndi mpingo. Iye ndiye chiyambi
chake, woyamba kuuka kwa akufa, kuti Iyeyo akhale wopambana zonse.
19 Pakuti kunamukomera Mulungu kuti umulungu wake wonse ukhalemo
mwa Khristu. 20 Ndipo kudzera mwa Iye Mulungu ayanjanitsenso zinthu
zonse ndi Iye mwini, zinthu za pa dziko lapansi, kapena zinthu za

kumwamba. Iye anachita mtendere kudzera m'magazi ake, wokhetsedwa
pa mtanda.
21 Kale inu munali kutali ndi Mulungu ndipo munali adani a Mulungu
m'maganizo mwanu chifukwa cha khalidwe lanu loyipa. 22 Koma
tsopano Iye anakuyanjanitsani m'thupi la Khristu kudzera mu imfa
kuti akuperekeni pamaso pake oyera, opanda banga ndi opanda chot-
sutsidwa nacho 23 ngati mupitirirabe kukhala m'chikhulupiriro chanu,
okhazikika ndi olimba, osasunthidwa kuchoka pa chiyembekezo chimene
munachigwira mu Uthenga Wabwino. Uwu ndi Uthenga Wabwino umene
munawumva, umene wakhala ukulalikidwa kwa olengedwa onse a pansi
pa thambo, ndi umenenso, ine Paulo ndinakhala mtumiki wake.

### *Utumiki wa Paulo ku Mpingo*

24 Tsopano ine ndikukondwa kuti ndinavutika chifukwa cha inu, ndipo
ndikukwaniritsa m'thupi langa zimene zikuperewera pa masautso a
Khristu, chifukwa cha thupi lake, limene ndi Mpingo. 25 Ine ndakhala
mtumiki wake mwa lamulo limene Mulungu anandipatsa kuti ndipereke
Mawu a Mulungu athunthu, 26 chinsinsi chimene chakhala chikubisika
kwa nthawi ndi mibado, koma tsopano chawululidwa kwa oyera mtima.
27 Kwa iwo amene Mulungu anawasankha kuti awadziwitse pakati pa a
mitundu ina, ulemerero wa chuma cha chinsinsi ichi, amene ndi Khristu
mwa inu, chiyembekezo cha ulemerero.
28 Ife tikulalikira Khristu, kulangiza ndi kuphunzitsa aliyense mwa nzeru
zonse kuti timupereke aliyense wangwiro mwa Khristu. 29 Ndi cholinga
chimenechi, ine ndikugwira ntchito molimbika ndi mwamphamvu zonse
zimene Iye anachita mwa ine.

## 2

1 Ndikufuna mudziwe kuti ndikukuvutikirani kwambiri, inuyo pamodzi
ndi anzanu a ku Laodikaya, ndi ena onse amene sitinaonane maso ndi
maso. 2 Cholinga changa n'chakuti alimbikitsidwe ndi kuyanjana pamodzi
m'chikondi, akhale odzaza ndi nzeru zomvetsa zinthu, ndi kuti azindikire
chinsinsi cha Mulungu, chimene ndi Khristu. 3 Mwa Iyeyu muli chuma
chonse chobisidwa cha nzeru ndi chidziwitso. 4 Ndikukuwuzani zimenezi
kuti wina aliyense asakunamizeni ndi kukukopani ndi mawu ake. 5 Pakuti
ngakhale sindili pakati panu m'thupi, ndili nanu pamodzi mu mzimu,
ndipo ndikukondwa kuona kuti mukulongosola bwino zonse ndiponso kuti
chikhulupiriro chanu mwa Khristu ndi chokhazikika ndithu.

### *Za Moyo Weniweni mwa Khristu*

6 Tsono popeza munavomereza Khristu Yesu kukhala Ambuye anu,
mupitirire kukhala mwa Iyeyo. 7 Mukhale ozikika mizu mwa Iye,
ndipo moyo wanu umangike pa Iye. Mulimbike m'chikhulupiriro monga
momwe munaphunzirira, ndipo kuyamika kwanu kusefukire.
8 Musalole kuti wina aliyense akutengeni ukapolo ndi m'nzeru
zachinyengo zolongosola zinthu zozama, zomwe zimachokera ku
miyambo ya anthu ndi ku maganizo awo okhudza za dziko lapansi osati
kwa Khristu.
9 Pakuti m'thupi la Khristu mumakhala umulungu wonse wathunthu.
10 Ndipo inunso ndinu athunthu mwa Khristu. Iye ndiye mtsogoleri wa
pamwamba pa maufumu onse ndi maulamuliro wonse. 11 Mwa Iye inunso
munachita mdulidwe m'thupi lanu, osati mdulidwe ochitidwa ndi manja
a anthu ayi, koma ochitidwa ndi Khristu pamene anavula khalidwe lanu

lauchimo lija. 12 Mu ubatizo, munayikidwa m'manda pamodzi ndi Khristu
ndi kuukitsidwa naye pamodzi, pokhulupirira mphamvu za Mulungu
amene anamuukitsa kwa akufa.
13 Pamene munali akufa chifukwa cha machimo anu ndi osachita
mdulidwe m'mitima mwanu, Mulungu anakupatsani moyo mwa Khristu.
Iye anatikhululukira machimo athu onse. 14 Anafafaniza kalata ya
ngongole yathu, pomwe panali milandu yotitsutsa ife. Iye anayichotsa,
nayikhomera pa mtanda. 15 Ndipo atalanda zida maufumu ndi maula-
muliro, Iye anawachititsa manyazi powayendetsa pamaso pa anthu onse
atawagonjetsa ndi mtanda.

### *Ufulu Wathu*

16 N'chifukwa chake musalole wina aliyense kukuzengani mlandu
chifukwa cha zimene mumadya kapena kumwa, kapena za masiku
achikondwerero cha chipembedzo, za chikondwerero cha mwezi wat-
sopano, kapena za tsiku la Sabata. 17 Zimenezi ndi chithunzithunzi chabe
cha zinthu zimene zikubwera, koma choonadi chenicheni chikupezeka
mwa Khristu. 18 Musalole kuti wina aliyense amene amakonda kudzichep-
etsa mwachiphamaso ndi kumapembedza angelo akulepheretseni kuka-
landira mphotho. Munthu woteroyu amayankhulanso mwatsatanetsatane
zinthu zimene akuti anaziona m'masomphenya. Anthuwa ndi odzituku-
mula ndi fundo zopanda pake zochokera m'maganizo mwawo amene si
auzimu. 19 Iwo sakulumikizananso ndi mutu, kumene kumachokera thupi
lonse, logwirizidwa ndi kumangiririridwa pamodzi ndi m'mitsempha yake
ndi mnofu, limene limakula monga mmene Mulungu afunira kuti likulire.
20 Popeza munafa pamodzi ndi Khristu kusiyana nayo miyambo ya dziko
lapansi lino, n'chifukwa chiyani mukukhalanso ngati a dziko lapansi lino?
Bwanji mukumvera malamulo monga awa: 21 "Usagwire chakuti," "Us-
alawe chakuti," "Usakhudze chakuti?" 22 Malamulo amenewa amakhudza
zinthu zimene zimatha zikamagwiritsidwa ntchito, ndipo malamulo ndi
zophunzitsa za anthu chabe. 23 Ndithu malamulo oterewa amaoneka
ngati anzeru, pakuti amalamulira anthu ambiri pa zachipembedzo ndi pa
zakudzichepetsa kwa chiphamaso, ndi pa zakuzunza thupi lawo, koma
alibe mphamvu zoletsa kuchita zofuna za thupilo.

## 3

### *Moyo Watsopano*

1 Tsono popeza munaukitsidwa pamodzi ndi Khristu, ikani mitima yanu
pa zinthu za kumwamba, kumene Khristu akukhala ku dzanja lamanja
la Mulungu. 2 Muzifunafuna zinthu za kumwamba, osati zinthu za pa
dziko lapansi. 3 Pakuti munafa, ndipo moyo wanu tsopano wabisika
pamodzi ndi Khristu mwa Mulungu. 4 Khristu, amene ndiye moyo
wanu, akadzaonekanso, pamenepo inunso mudzaoneka naye pamodzi mu
ulemerero.
5 Choncho, iphani zilakolako za dziko lapansi mwa inu, monga: dama,
zodetsa, kulakalaka zosayenera, kukhumba zoyipa ndi umbombo, pakuti
umbombo ndiko kupembedza mafano. 6 Chifukwa cha zimenezi, mkwiyo
wa Mulungu ukubwera pa ana osamvera. 7 Inunso kale munkachita
zomwezi, m'moyo wanu wakale uja. 8 Koma tsopano mukuyenera
kuzichotsa zinthu zonsezi monga: mkwiyo, ukali, dumbo, chipongwe ndi
mawu onyansa. 9 Musanamizane wina ndi mnzake, popeza munavula

munthu wakale pamodzi ndi zochita zake 10 ndipo mwavala munthu
watsopano, amene nzeru zake zikukonzedwanso kuti afanane ndi Mlengi
wake. 11 Pano palibe kusiyana pakati pa Mgriki ndi Myuda, wochita
mdulidwe ndi wosachita, wosaphunzira kapena wosachangamuka, kapolo
kapena mfulu, koma Khristu yekha basi ndipo amakhala mwa onse.

12 Choncho, ngati anthu osankhidwa ndi Mulungu, oyera mtima ndi
okondedwa kwambiri, muvale chifundo, kukoma mtima, kudzichepetsa,
kufatsa ndi kupirira. 13 Mulezerane mtima ndipo muzikhululukirana ngati
wina ali ndi chifukwa ndi mnzake. Muzikhululukirana monga Ambuye
anakhululukira inu. 14 Ndipo kuwonjezera pa zonsezi valani chikondi,
chimene chimangirira zonsezi pamodzi mu mgwirizano wangwiro.

15 Mtendere wa Khristu ulamulire m'mitima mwanu, popeza monga
ziwalo za thupi limodzi, munayitanidwa kuti mukhale ndi mtendere.
Ndipo muziyamika. 16 Mawu a Khristu akhazikike kwathunthu m'mitima
mwanu. Muziphunzitsana ndi kulangizana wina ndi mnzake ndi nzeru
zonse pamene mukuyimba Masalimo, nyimbo zotamanda ndi nyimbo
zauzimu, kuyimbira Mulungu ndi mitima yoyamika. 17 Ndipo chilichonse
chimene mungachite, kaya n'kuyankhula, kaya n'kugwira ntchito, mu-
chite zonse m'dzina la Ambuye Yesu, kuyamika kwa Mulungu Atate
kudzera mwa Iye.

### *Malangizo a Moyo wa M'banja la Chikhristu*

18 Inu akazi, gonjerani amuna anu, monga kuyenera mwa Ambuye.

19 Inu amuna, kondani akazi anu ndipo musawapsere mtima.

20 Inu ana, mverani makolo anu mu zonse pakuti izi zimakondweretsa
Ambuye.

21 Inu abambo, musakwiyitse ana anu, kuti angataye mtima.

22 Inu antchito, mverani mabwana anu mu zonse, ndipo muzichita
zimenezi osati nthawi yokhayo imene akukuonani kuti akukondeni, koma
muzichite moona mtima ndi mopereka ulemu kwa Ambuye. 23 Chilichonse
mungachite, muchite ndi mtima wanu onse, monga mmene mungagwirire
ntchito ya Ambuye osati ya anthu. 24 Inu mukudziwa kuti mudzalandira
mphotho monga cholowa kuchokera kwa Ambuye. Ndi Ambuye Khristu
amene mukumutumikira. 25 Aliyense amene amachita zolakwa adza-
landira malipiro molingana ndi kulakwa kwake, ndipo palibe tsankho.

## 4

1 Mabwana, antchito anu muzikhala nawo mwachilungamo ndi moyen-
era, podziwa kuti nanunso muli nawo Ambuye anu mmwamba.

### *Malangizo Ena*

2 Pempherani modzipereka, mukhale atcheru ndiponso oyamika.
3 Ndipo muzitipempherereranso ife kuti Mulungu atitsekulire khomo la
uthenga wathu, kuti tilalikire chinsinsi cha Khristu, chimene ndine
womangidwa nacho m'ndende. 4 Pempherani kuti ndilalikire momveka
bwino, monga ndikuyenera. 5 Mayendedwe anu pakati pa akunja, akhale
anzeru ndipo mugwiritse ntchito mpata uliwonse umene muli nawo.
6 Mayankhulidwe anu nthawi zonse akhale odzaza ndi chisomo ndi okoma,
kuti mudziwe kuyankha aliyense.

### *Mawu Otsiriza*

7 Tukiko adzakuwuzani zonse za ine. Iye ndi m'bale wokondedwa,
mtumiki wokhulupirika ndiponso wantchito mnzanga mwa Ambuye. 8 Ine
ndikumutumiza kwa inu ndi cholinga choti mudziwe zimene tikukumana
nazo ndiponso kuti alimbikitse mitima yanu. 9 Iye akubwera ndi Onesimo,
m'bale wathu wokhulupirika ndi wokondedwa, amene ndi mmodzi mwa
inu. Iwo adzakuwuzani zonse zimene zikuchitika kuno.

10 Aristariko, wam'ndende mnzanga akupereka moni, Marko aku-
perekanso moni, msuweni wa Barnaba. (Inu munawuzidwa kale za
Iye. Iye akabwera kwanuko, mulandireni). 11 Yesu wotchedwa Yusto,
akuperekanso moni. Amenewa ndi Ayuda okhawo pakati pa atumiki
anzanga mu ufumu wa Mulungu, ndipo aonetsa kuti ndi chitonthozo
kwa ine. 12 Epafra ndi mmodzi mwa inu ndiponso mtumiki wa
Khristu Yesu, akupereka moni. Iyeyu nthawi zonse amakupempharerani
mwamphamvu, kuti mukhazikike pa chifuniro chonse cha Mulungu,
mukhale okhwima ndi otsimikiza kwathunthu. 13 Ine ndikumuchitira
umboni kuti amagwira ntchito mwamphamvu chifukwa cha inu ndiponso
kwa amene ali ku Laodikaya ndi Herapoli. 14 Luka, dotolo wathu
wokondedwa ndi Dema, akupereka moni. 15 Perekani moni kwa abale
a ku Laodikaya, ndiponso kwa Numfa ndi mpingo wa m'nyumba mwake.

16 Kalata iyi ikawerengedwa pakati panu, muonetsetse kuti ikaw-
erengedwenso ku mpingo wa ku Laodikaya ndipo inunso muwerenge
kalata yochokera ku Laodikaya.

17 Uzani Arkipo kuti, "Wonetsetsa kuti wamaliza ntchito imene unayi-
landira mwa Ambuye."

18 Ine Paulo, ndikulemba ndi dzanja langa moni uwu. Kumbukirani kuti
ndili mu unyolo. Chisomo chikhale ndi inu.

# KALATA YOYAMBA YA PAULO YOLEMBERA ATESALONIKA

1 Paulo, Silivano ndi Timoteyo.
Tikulembera mpingo wa ku Tesalonika, umene uli mwa Mulungu Atate ndi Ambuye Yesu Khristu.
Chisomo ndi mtendere kwa inu.

*Kuyamikira Chikhulupiriro cha Atesalonika*

2 Ife timayamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu. Timakutchu-
lani m'mapemphero athu. 3 Nthawi zonse timakumbukira ntchito yanu
yachikhulupiriro, yachikondi ndi kupirira kwanu kwa chiyembekezo mwa Ambuye athu Yesu Khristu, pamaso pa Mulungu wathu ndi Atate.
4 Abale okondedwa ndi Mulungu, tikudziwa kuti Mulungu anaku-
sankhani, 5 chifukwa uthenga wathu wabwino sunafike kwa inu ndi mawu
okha, koma ndi mphamvu za Mzimu Woyera ndi chitsimikizo chachikulu.
Mukudziwa mmene tinkakhalira pakati panu kuti tikuthandizeni. 6 Inu
mwakhala otitsatira athu ndi a Ambuye; ngakhale kuti panali masautso akulu, munalandira uthenga mwachimwemwe chochokera kwa Mzimu
Woyera. 7 Ndipo potero munakhala chitsanzo kwa abale onse a ku
Makedoniya ndi Akaya. 8 Kuchokera kwa inu, uthenga wa Ambuye
unamveka ku Makedoniya ndi ku Akaya ndipo mbiri ya chikhulupiriro chanu mwa Mulungu yamveka ponseponse. Choncho sikofunikanso kuti
tinene kanthu, 9 pakuti iwo amafotokoza za momwe munatilandirira. Iwo
amatiwuza za momwe munatembenukira kwa Mulungu kusiya mafano
ndi kutumikira Mulungu wamoyo ndi woona. 10 Ndipo mukudikira
Mwana wake kuchokera kumwamba, Yesu, amene Mulungu anamuukitsa kwa akufa. Iyeyo amatipulumutsa ku mkwiyo umene ukubwera.

## 2

*Utumiki wa Paulo ku Atesalonika*

1 Abale, mukudziwa kuti kudzacheza kwathu kwa inu sikunali kosapin-
dulitsa. 2 Monga mukudziwa, ife n'kuti titazunzika ndi kunyozedwa ku
Filipi. Koma mothandizidwa ndi Mulungu wathu, tinalimba mtima mpaka kukulalikirani uthenga wake wabwino ngakhale ambiri ankatsutsana
nafe. 3 Pakuti kulalikira kumene tikuchita, sitikuchita ndi maganizo olak-
wika kapena zolinga zoyipa, kapenanso kufuna kukunamizani. 4 Koma
timayankhula monga anthu ovomerezeka ndi Mulungu ndi osungitsidwa Uthenga Wabwino. Ife sitikufuna kukondweretsa anthu koma Mulungu,
amene amasanthula mitima yathu. 5 Monga mukudziwa kuti sitinag-
wiritse ntchito mawu oshashalika kapena mtima wofuna phindu, Mulungu
ndiye mboni yathu. 6 Ife sitinafune kutamidwa ndi anthu, kapena ndi
inu, kapena wina aliyense mwa inu. 7 Ngati atumwi a Khristu tikanatha
kukhala cholemetsa kwa inu, m'malo mwake tinali ngati ana aang'ono pakati panu.
Monga mmene amayi amasamalira ana awo ang'ono, 8 moteronso
tinakusamalirani. Chifukwa tinakukondani kwambiri, tinali okondwa kugawana nanu osati Uthenga Wabwino wa Mulungu wokha, komanso
miyoyo yathu. 9 Abale, pakuti mukumbukira kugwira ntchito kwathu

kwambiri ndi kuvutika; ife tinagwira ntchito usana ndi usiku ndi cholinga
chakuti tisakhale cholemetsa, kwa aliyense pamene ife tinkalalikira
Uthenga Wabwino wa Mulungu kwa inu.
10 Inu ndinu mboni, ndiponso Mulungu, kuti tinali oyera mtima,
olungama ndi wopanda chifukwa pakati panu amene munakhulupirira.
11 Monga mudziwa kuti ife tinkasamala aliyense wa inu monga abambo
amasamalira ana ake, 12 kulimbikitsa, kutonthoza ndi kukupemphani kuti
mukhale moyo oyenera Mulungu amene anakuyitanani kuti mulowe mu
ufumu wake ndi ulemerero.
13 Ndipo ifenso tikuyamika Mulungu kosalekeza chifukwa mutalandira
Mawu a Mulungu, amene munawamva kuchokera kwa ife, munawa-
landira osati ngati mawu a anthu, koma monga momwe alili, Mawu
a Mulungu, amene akugwira ntchito mwa inu amene mukhulupirira.
14 Pakuti inu abale, munakhala otsanzira mipingo ya Mulungu ya
ku Yudeya, imene ili mwa Khristu Yesu. Munasautsidwa kuchokera
kwa anthu a mtundu wanu, zinthu zomwezo zimene mipingo imeneyi
inasautsidwa ndi Ayuda, 15 amene anapha Ambuye Yesu ndi aneneri ndipo
anatithamangitsanso ife. Iwo sakondweretsa Mulungu ndipo amadana
ndi anthu onse 16 ndikutiretsa ife kuti tisayankhule ndi a mitundu ina
kuti angapulumuke. Motero iwo amadziwunjikira okha machimo awo.
Mkwiyo wa Mulungu wa afikira tsopano.

### *Paulo Afunitsitsa Kuonanso Atesalonika*

17 Koma abale, titasiyana kwa nthawi pang'ono (m'thupi osati
m'maganizo), tinayesetsa koposa kuti tikuoneni. 18 Pakuti ife tinafuna
kubweranso kwa inu, makamaka ine Paulo, ndinayesa kangapo koma
Satana anatiletsa. 19 Nanga chiyembekezo chathu, chimwemwe chathu
kapena chaufumu chimene ife tidzanyadira pamaso pa Ambuye athu Yesu
Khristu pamene abwere ndi chiyani? Kodi si inu? 20 Indedi, inu ndinu
ulemerero wathu ndi chimwemwe.

## 3

1 N'chifukwa chake pamene sitinathenso kupirira, tinaganiza kuti
kunali bwino kuti atisiye tokha ku Atene. 2 Tinatuma Timoteyo, m'bale
wathu ndi mnzathu wogwira naye ntchito ya Mulungu yofalitsa Uthenga
Wabwino wa Khristu, kuti adzakulimbitseni mitima ndi kukukhazikitsani
m'chikhulupiriro chanu, 3 ndi cholinga chakuti wina asasunthike ndi
mavutowa. Inu mukudziwa bwino lomwe kuti ndife oyenera kukumana
ndi zimenezi. 4 Kunena zoona, pamene tinali nanu, tinkakuwuzani kuti
tidzayenera kuzunzidwa. Ndipo monga mukudziwa bwino, zimenezi
zinachitikadi. 5 N'chifukwa chake, pamene sindikanathanso kupirira,
ndinatuma Timoteyo kuti adzaone mmene chikhulupiriro chanu chilili.
Ndinkaopa kuti mwina wonyengayo, wakunyengani m'njira ina yake ndi
kuti ntchito zathu zasanduka zosapindula.

### *Nkhani Yolimbikitsa Kuchokera kwa Timoteyo*

6 Koma tsopano Timoteyo wabwera kuchokera kwanuko ndipo watib-
weretsera nkhani yabwino ya chikhulupiriro chanu ndi chikondi chanu.
Iye watiwuzanso kuti masiku onse mumatikumbukira mokondwa, ndipo
kuti mumafunitsitsa kutionanso, monga momwe ifenso timalakalakira
kukuonani inuyo. 7 Motero abale, m'masautso ndi m'mazunzo athu
onse, chikhulupiriro chanu chatilimbikitsa. 8 Ife tsopano tili moyodi,

pakuti mukuyima molimbika mwa Ambuye. 9 Tingathe bwanji kuyamika
Mulungu mokwanira poona chimwemwe chonse chimene tili nacho
pamaso pa Mulungu wathu chifukwa cha inu? 10 Usana ndi usiku
timapemphera ndi mtima wonse kuti tionanenso nanu, ndi kukwaniritsa
zimene zikusowa pa chikhulupiriro chanu.
11 Tikupempha kuti Mulungu ndi Atate athu mwini, ndi Ambuye athu
Yesu, atikonzere njira yabwino kuti tidzafike kwanuko. 12 Ambuye
achulukitse chikondi chanu ndi kuti chisefukire kwa wina ndi mnzake
ndiponso kwa wina aliyense, monga momwe chikondi chathu chichitira
kwa inu. 13 Iye alimbikitse mitima yanu kuti mukhale opanda cholakwa
ndi oyera mtima pamaso pa Mulungu ndi Atate athu pamene Ambuye athu
Yesu akubwera ndi oyera ake onse.

# 4

### *Moyo Wokondweretsa Mulungu*

1 Potsiriza, abale, tinakulangizani kale momwe mukuyenera kukhalira
kuti mukondweretse Mulungu, monga momwe mukukhaliramo. Tsopano
tikukupemphani ndi kukulimbikitsani mwa Ambuye Yesu kuti muchite
zimenezi koposa kale. 2 Inu mukudziwa malangizo amene tinakupatsani
mwa ulamuliro wa Ambuye Yesu.
3 Ndi chifuniro cha Mulungu kuti muyeretsedwe: kuti mupewe dama;
4 aliyense wa inu aphunzire kulamulira thupi lake m'njira yoyera ndi
yaulemu, 5 osati yotsata chilakolako chonyansa monga amachitira akunja,
amene sadziwa Mulungu. 6 Pa zimenezi munthu asachimwire m'bale
wake kapena kumuonerera. Ambuye adzalanga anthu onse amene
amachita machimo amenewa, monga tinakuwuzani kale ndi kukuchen-
jezani. 7 Pakuti Mulungu sanatiyitane kuti tizichita zonyansa, koma kuti
tikhale oyera mtima. 8 Choncho, aliyense amene akukana malangizo
awa sakukana munthu koma Mulungu, Mulungu weniweniyo amene
amakupatsani Mzimu Woyera.
9 Tsono kunena za kukondana wina ndi mnzake, n'kosafunikira kuti
tikulembereni, popeza ndi Mulungu amene anakuphunzitsani za kukon-
dana wina ndi mnzake. 10 Ndipo kunena zoona, mumakonda abale onse a
m'banja la Mulungu a ku Makedoniya. Komabe, abale tikukulimbikitsani
kuti muzichita zimenezi koposa kale.
11 Yesetsani kuti mukhale moyo wofatsa. Aliyense asamale ntchito
yakeyake ndi kugwira ntchito ndi manja ake. 12 Mukatero akunja
adzalemekeza makhalidwe anu a tsiku ndi tsiku, ndi kuti inuyo mukhale
osadalira wina aliyense.

### *Kubweranso kwa Ambuye*

13 Abale, ife sitikufuna mukhale osadziwa za amene akugona,
kapena kumva chisoni ngati anthu ena opanda chiyembekezo.
14 Ife timakhulupirira kuti Yesu anamwalira naukanso. Moteronso
timakhulupirira kuti amene anamwalira ali mwa Yesu, Mulungu
adzawaukitsa n'kubwera nawo pamodzi ndi Yesuyo. 15 Molingana
ndi mawu a Ambuye mwini, tikukuwuzani kuti, ife amene tikanali ndi
moyo, otsala mpaka kubwera kwa Ambuye, sitidzawasiya kumbuyo
amene anagona kale. 16 Pakuti Ambuye mwini adzatsika kuchokera
kumwamba, ndi mfuwu waulamuliro, ndi liwu la mngelo wamkulu, ndi
kulira kwa lipenga la Mulungu, ndipo akufa amene ali mwa Yesu adzauka

poyamba. 17 Kenaka, ife amene tili ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa
pamodzi ndi iwo m'mitambo kukakumana ndi Ambuye mlengalenga.
Tsono ife tidzakhala ndi Ambuye mpaka muyaya. 18 N'chifukwa chake
tsono muzilimbikitsana ndi mawu amenewa.

# 5

*Tsiku la Ambuye*

1 Tsono abale, za nthawi ndi nyengo yake n'kosafunikira kuti tikulem-
bereni, 2 chifukwa mukudziwa bwino lomwe kuti tsiku la Ambuye
lidzafika ngati mbala usiku. 3 Pamene anthu akunena kuti, "Mtendere
ndi chitetezo," chiwonongeko chidzafika pa iwo mwadzidzidzi, monga
zowawa za amayi pobereka, ndipo sadzathawa.
4 Koma inu abale, simuli mu mdima kuti tsiku limeneli lidzakudzidz-
imutseni ngati mbala. 5 Nonse ndinu ana a kuwunika ndi ana a usana.
Sindife anthu a usiku kapena mdima. 6 Chomwecho tsono, tisafanane
ndi ena amene akugona koma tikhale maso ndi odzisunga. 7 Pakuti
amene akugona, amagona usiku, ndi amene amaledzera, amaledzera
usiku. 8 Koma popeza ndife a usana, tikhale odzisunga, titavala
chikhulupiriro ndi chikondi ngati chovala pachifuwa, ndi chiyembekezo
cha chipulumutso ngati chipewa. 9 Pakuti Mulungu sanatisankhe kuti
tikavutike ndi mkwiyo koma kuti tilandire chipulumutso kudzera mwa
Ambuye athu Yesu Khristu. 10 Iye anatifera ndi cholinga chakuti, kaya tili
ndi moyo kapena tagona, tikhale naye pamodzi. 11 Choncho limbikitsanani
wina ndi mnzake ndi kuthandizana kukula mu mzimu, monga momwe
mukuchitira.

*Malangizo Otsiriza*

12 Tsopano tikukupemphani abale kuti muziwalemekeza amene akug-
wira ntchito pakati panu, amene amakuyang'anirani mwa Ambuye
ndi amene amakulimbikitsani. 13 Muziwachitira ulemu kwambiri
mwachikondi chifukwa cha ntchito yawo. Mukhale pa mtendere wina
ndi mnzake. 14 Ndipo tikukupemphani abale, muwachenjeze amene akun-
gokhala osagwira ntchito, alimbikitseni amanyazi, thandizani ofowoka
ndipo muzilezera mtima aliyense. 15 Onetsetsani kuti wina asabwezere
choyipa kwa omuchitira choyipa koma nthawi zonse yesetsani kukhala
okoma mtima kwa wina ndi mnzake; ndiponso ndi kwa anthu ena onse.
16 Kondwerani nthawi zonse. 17 Pempherani kosalekeza. 18 Yamikani mu
zonse, pakuti ichi ndi chifuniro cha Mulungu kwa inu mwa Khristu Yesu.
19 Musazimitse moto wa Mzimu Woyera. 20 Musanyoze mawu a uneneri.
21 Yesani zinthu zonse. Gwiritsitsani chimene ndi chabwino. 22 Mupewe
choyipa cha mtundu wina uliwonse.
23 Mulungu mwini, Mulungu wamtendere, akuyeretseni kotheratu.
Mzimu wanu wonse, moyo ndi thupi zisungidwe zopanda cholakwa
mpaka kubwera kwa Ambuye athu Yesu Khristu. 24 Amene anakuyitanani
ndi wokhulupirika ndipo Iye adzachita zimenezi.
25 Abale, mutipempherere. 26 Perekani moni wachikondi kwa onse.
27 Pamaso pa Ambuye ndikulamula kuti kalatayi iwerengedwe kwa abale
onse.
28 Chisomo cha Ambuye athu Yesu Khristu chikhale nanu.

# KALATA YACHIWIRI YA PAULO YOLEMBERA ATESALONIKA

1 Paulo, Silivano ndi Timoteyo.

Kulembera mpingo wa ku Tesalonika, umene uli mwa Mulungu Atate athu ndi Ambuye Yesu Khristu.

2 Chisomo ndi mtendere kwa inu kuchokera kwa Mulungu Atate ndi Ambuye Yesu Khristu.

### *Kuyamika ndi Pemphero*

3 Ife tiyenera kuyamika Mulungu nthawi zonse chifukwa cha inu
abale. Ndipo tiyenera kutero chifukwa chikhulupiriro chanu chikukuli-
rakulirabe, ndiponso chikondi chimene aliyense wa inu ali nacho pa
mnzake chikuchulukirachulukirabe. 4 N'chifukwa chake, timayankhula
monyadira m'mipingo yonse ya Mulungu za kupirira kwanu ndi
chikhulupiriro chanu pakati pa masautso onse ndi mayesero amene
mukudutsamo.
5 Zonsezi zikutsimikiza kuti Mulungu amaweruza molungama. Zotsatira
zake ndi zakuti mudzatengedwa kukhala oyenera kulowa mu ufumu
wa Mulungu umene mukuwuvutikira. 6 Mulungu ndi wolungama
ndipo adzalanga amene amakusautsaniwo 7 ndikukupatsani mpumulo
amene mukusautsidwa, pamodzi ndi ifenso. Izi zidzachitika Ambuye
Yesu akadzaoneka m'malawi amoto kuchokera kumwamba pamodzi
ndi angelo ake amphamvu. 8 Iye adzalanga amene sadziwa Mu-
lungu ndi amene samvera Uthenga Wabwino wa Ambuye athu Yesu.
9 Adzalangidwa ndi chiwonongeko chamuyaya ndipo sadzaonanso nkhope
ya Ambuye ndi ulemerero wamphamvu zake 10 pa tsiku limene iye
adzabwera kudzalemekezedwa mwa oyera mtima ndi kuyamikidwa ndi
onse amene anakhulupirira. Inu mudzakhala nawo m'gulumo chifukwa
munakhulupirira umboni wathu.
11 N'chifukwa chake timakupemphererani nthawi zonse, kuti Mulungu
wathu akusandutseni oyenera mayitanidwe ake, ndi kuti mwa mphamvu
zake akwaniritse cholinga chanu chilichonse chabwino ndi chilichonse
chochitika mwachikhulupiriro. 12 Ife timapempherera zimenezi kuti dzina
la Ambuye athu Yesu lilemekezedwe mwa inu, ndi inu mulemekezedwe
mwa Iyeyo. Zonsezi zidzachitika chifukwa cha chisomo cha Mulungu
wathu ndi Ambuye Yesu Khristu.

## 2

### *Kubwera kwa Munthu Woyipitsitsa*

1 Pa za kubweranso kwa Ambuye athu Yesu Khristu ndiponso za
kusonkhana kwathu kuti tikumane naye, abale, tikukupemphani 2 kuti
musagwedezeke msanga m'maganizo kapena kuopsezedwa ndi uneneri,
mbiri kapena kalata yokhala ngati yachokera kwa ife, yonena kuti tsiku lija
la Ambuye linafika kale. 3 Musalole kuti wina aliyense akunamizeni mwa
njira ina iliyonse. Pakuti tsikulo lisanafike, kudzakhala mpatuko waukulu
kwambiri, ndipo kudzaoneka munthu woyipitsitsa uja, munthu woyenera

kuwonongedwayo. 4 Iyeyo adzatsutsa ndi kudziyika pamwamba pa chili-
chonse chimene anthu amachitcha mulungu kapena amachipembedza.
Iyeyo adzadzikhazika m'Nyumba ya Mulungu ndi kudzitcha Mulungu.
5 Kodi simukukumbukira kuti pamene ndinali nanu pamodzi
ndinkakuwuzani zimenezi? 6 Ndipo tsopano mukudziwa chimene
chikumuletsa kuonekera, koma adzawululika pa nthawi yake yoyenera.
7 Pakuti mphamvu yobisika yoyipitsitsa ikugwira ntchito ngakhale
tsopano; koma amene akutchinga mphamvuyo adzapitiriza kutero mpaka
pamene wotchingayo adzachotsedwe. 8 Ndipo kenaka woyipitsitsayo
adzaonekera, amene Ambuye Yesu adzamugonjetsa ndi mpweya otuluka
m'kamwa mwake ndi kumuwononga ndi ulemerero wa kubwera kwake.
9 Woyipitsitsayo adzabwera ndi mphamvu za Satana. Adzaonetsa
mphamvu zake pochita zizindikiro ndi zodabwitsa zachinyengo. 10 Iye
adzagwiritsa ntchito mtundu uliwonse wachinyengo kupusitsa amene
akuwonongeka. Iwo akuwonongeka chifukwa akukana kukonda
choonadi ndi kuti apulumutsidwe. 11 Chifukwa cha chimenechi, Mulungu
akuwatumizira chinyengo chachikulu kuti akhulupirire bodza. 12 Choncho
adzalangidwa onse amene sanakhulupirire choonadi, koma anakondwera
mu zoyipa.

### *Imani Mwamphamvu*

13 Koma tiyenera kuyamika Mulungu chifukwa cha inu abale okond-
edwa mwa Ambuye, pakuti Mulungu anakusankhani pachiyambi pomwe
kuti mupulumuke chifukwa cha ntchito yoyeretsa ya Mzimu ndi
chikhulupiriro chanu m'choonadi. 14 Iye anakuyitanirani zimenezi
kudzera mwa uthenga wathu wabwino, kuti mulandire nawo ule-
merero wa Ambuye athu Yesu Khristu. 15 Kotero tsono, abale, imani
mwamphamvu ndi kugwiritsa ziphunzitso zimene tinakupatsani kudzera
m'mawu apakamwa kapena kudzera m'kalata.
16 Ambuye athu Yesu Khristu mwini ndi Mulungu Atate wathu, amene
anatikonda ife ndipo mwachisomo chake anatipatsa kulimba mtima kwa-
muyaya ndi chiyembekezo chabwino, 17 akulimbikitseni ndi kukupatsani
mphamvu yogwirira ntchito ndi kuyankhula zabwino zilizonse.

## 3

### *Tipempherereni*

1 Potsiriza, abale, mutipempherere kuti uthenga wa Ambuye ufalikire
msanga ndi kulemekezedwa monga momwe munachitira inu. 2 Ndipo
pempherani kuti tilanditsidwe m'manja mwa anthu ovuta ndi oyipa,
pakuti si onse amene ali nacho chikhulupiriro. 3 Koma Ambuye ndi
wokhulupirika, ndipo adzakulimbikitsani ndi kukutetezani kwa woyipayo.
4 Tili ndi chikhulupiriro mwa Ambuye kuti mukuchita zonse ndipo
mudzapitirira kuchita zimene tinakulamulirani. 5 Ambuye atsogolere
mitima yanu kuti mudziwe chikondi cha Mulungu ndiponso kupirira
kumene Khristu amapereka.

### *Awachenjeza za Kusagwira Ntchito*

6 Abale, tikukulamulani m'dzina la Ambuye Yesu Khristu, kuti mupewe
m'bale aliyense amene ndi waulesi ndi wachisokonezo, wosafuna kutsata
zimene tinakuphunzitsani. 7 Pakuti inu mukudziwa zimene muyenera
kuchita pofuna kutitsatira. Ife sitinali alesi pamene tinali nanu 8 ndipo

sitinadye chakudya cha aliyense osalipira. Komatu tinkagwira ntchito
mwamphamvu usiku ndi usana kuti tisakhale cholemetsa kwa aliyense.
9 Sitinachite zimenezi chifukwa choti tinalibe mphamvu zolamula kuti
mutithandize koma kuti tikhale chitsanzo choti mutsatire. 10 Pakuti
ngakhale pamene tinali nanu, tinakupatsani lamulo lakuti, "Munthu
wosafuna kugwira ntchito, asadye."

11 Ife tikumva kuti pakati panu pali ena amene ndi alesi. Iwo safuna
kugwira ntchito, koma amangolowerera pa za eni. 12 M'dzina la Ambuye
Yesu Khristu, tikuwalamula ndi kuwakakamiza kuti azigwira ntchito
mwabata ndi kumadya chakudya chodzigwirira ntchito okha. 13 Koma
inu abale, musatope n'kuchita zabwino.

14 Ngati wina aliyense akana kumvera malangizo athu a m'kalatayi,
mumuonetsetse ameneyo ndipo musayanjane naye kuti achite manyazi.
15 Komatu musamutenge kukhala mdani, koma muchenjezeni ngati
m'bale.

### *Malonje Otsiriza*

16 Tsopano Ambuye mwini mtendere akupatseni mtendere nthawi zonse
mwa njira iliyonse. Ambuye akhale ndi inu nonse.

17 Ine Paulo, ndikulemba malonje awa ndi dzanja langa, chimene
ndi chizindikiro chodziwika m'makalata anga onse. Umo ndi mmene
ndimalembera.

18 Chisomo cha Ambuye athu Yesu Khristu chikhale ndi inu nonse.

# KALATA YOYAMBA YA PAULO YOLEMBERA TIMOTEYO

1 Paulo, mtumwi wa Khristu Yesu mwa lamulo la Mulungu, Mpulumutsi
wathu ndiponso Khristu Yesu chiyembekezo chathu.
2 Kwa Timoteyo mwana wanga weniweni m'chikhulupiriro.
Chisomo, chifundo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate ndi
Khristu Yesu Ambuye athu zikhale ndi iwe.

### *Kutsutsa Aphunzitsi Onyenga*

3 Monga ndinakupempha pamene ndinkapita ku Makedoniya, khala ku
Efeso komweko kuti uletse anthu ena kuphunzitsa ziphunzitso zonyenga,
4 kapena kumangoyika mitima pa nthano zopeka ndi kufufuza za mayina a
makolo awo. Zinthu zotere zimapititsa m'tsogolo mikangano m'malo mwa
ntchito ya Mulungu yomwe ndi ya chikhulupiriro. 5 Cholinga cha lamuloli
ndi chikondi, chomwe chimachokera mu mtima woyera, chikumbumtima
chabwino ndi chikhulupiriro choona. 6 Anthu ena anapatuka pa zimenezi
ndipo anatsata nkhani zopanda tanthauzo. 7 Iwo amafuna kukhala
aphunzitsi amalamulo, koma sadziwa zimene akunena, kapena zimene
akufuna kutsimikiza.
8 Tikudziwa kuti Malamulo ndi abwino ngati munthu awagwiritsa
ntchito bwino. 9 Tikudziwanso kuti Malamulo sakhazikitsidwa chifukwa
cha anthu olungama, koma ophwanya lamulo ndi owukira, osaopa
Mulungu ndi ochimwa, wopanda chiyero ndi osapembedza; amene
amapha abambo awo ndi amayi awo, kapena anthu ena. 10 Malamulo
amayikidwa chifukwa cha anthu achigololo ndi ochita zadama ndi amuna
anzawo, anthu ogulitsa akapolo, abodza ndi olumbira zabodza, ndi
ochita chilichonse chotsutsana ndi chiphunzitso choona. 11 Chiphunzitso
chimene chimagwirizana ndi Uthenga Wabwino wonena za ulemerero wa
Mulungu wodala, umene Iye mwini anandisungitsa.

### *Chisomo cha Ambuye kwa Paulo*

12 Ndikuthokoza Khristu Yesu Ambuye athu, amene anandipatsa
mphamvu pa ntchitoyi. Iye ananditenga kukhala wokhulupirira,
nandipatsa ntchito mu utumiki wake. 13 Ngakhale kuti kale ndinali
wachipongwe, wozunza ndi wankhanza, anandichitira chifundo chifukwa
ndinkachita mwaumbuli ndi mopanda chikhulupiriro. 14 Chisomo cha Am-
buye athu chinatsanulidwa pa ine mochuluka, pamodzi ndi chikhulupiriro
ndi chikondi zimene zili mwa Khristu Yesu.
15 Mawu odalirika ndi woyenera kuwavomereza kwathunthu ndi awa:
Yesu Khristu anabwera pa dziko lapansi kudzapulumutsa ochimwa, ndipo
mwa iwowo ine ndiye wochimwitsitsa. 16 Ndipo pa chifukwa chimenechi,
Mulungu anandichitira chifundo, kuti mwa ine, wochimwitsitsa, Khristu
Yesu aonetse kuleza mtima kwake konse kuti ndikhale chitsanzo cha omwe
angathe kumukhulupirira ndi kulandira moyo wosatha. 17 Tsopano kwa
Mfumu yamuyaya, yosafa, yosaoneka, amene Iye yekha ndiye Mulungu,
kukhale ulemu ndi ulemerero mpaka muyaya. Ameni.

### *Ntchito ya Timoteyo*

18 Mwana wanga Timoteyo, ndikukupatsa langizo ili molingana
ndi maulosi amene aneneri ananena za iwe. Pamene ukumbukira

mawu amenewa udzatha kumenya bwino nkhondo 19 utagwiritsitsa
chikhulupiriro ndi chikumbumtima chabwino. Ena anazikana zimenezi
motero chikhulupiriro chawo chinawonongeka. 20 Ena mwa amenewa
ndi Humenayo ndi Alekisandro, amene ndinawapereka kwa Satana kuti
aphunzire kusachita chipongwe Mulungu.

# 2

*Malangizo Achipembedzo*

1 Tsono choyamba ndikukupemphani kuti mupempherere anthu onse.
Mapemphero anu akhale opemba, opempha, opempherera ena ndi
oyamika. 2 Mupempherere mafumu ndi onse aulamuliro, kuti tikhale
moyo wamtendere ndi bata, woopa Mulungu ndi oyera mtima. 3 Izi ndi
zabwino ndipo zimakondweretsa Mulungu Mpulumutsi wathu, 4 amene
amafuna kuti anthu onse apulumutsidwe ndipo kuti adziwe choonadi.
5 Pakuti pali Mulungu mmodzi yekha ndi M'khalapakati mmodzi yekha
pakati pa Mulungu ndi anthu, munthu uja Khristu Yesu. 6 Iyeyu
anadzipereka kukhala dipo lowombolera anthu onse. Umenewu ndi
umboni umene waperekedwa mu nthawi yake yoyenera. 7 N'chifukwa
chake anandisankha kukhala mlaliki ndiponso mtumwi wophunzitsa
anthu a mitundu ina mawu achikhulupiriro choona. Sindikunama ayi,
ndikunena zoona.

8 Choncho ndikufuna kuti paliponse popemphera, amuna azikweza
manja awo kwa Mulungu mopanda mkwiyo kapena kukangana.

9 Ndikufunanso kuti amayi azivala mwaulemu, modzilemekeza ndi
moyenera. Adzikongoletse koma osati ndi tsitsi loluka mowonjeza muyeso
kapena zokongoletsa zagolide kapena mikanda yamtengowapatali kapena
ndi zovala zamtengowapatali. 10 Koma adzikongoletse ndi ntchito zabwino
zoyenera mayi wopembedza Mulungu.

11 Amayi azikhala chete pophunzitsidwa ndi mtima ogonjera
kwathunthu. 12 Ine sindikulola kuti amayi aziphunzitsa kapena
kulamulira amuna; koma akhale chete. 13 Pakuti Adamu ndiye
anayamba kupangidwa kenaka Hava. 14 Ndipo Adamu si amene
ananyengedwa koma mkazi ndiye amene ananyengedwa nachimwa.
15 Ndipo mkazi adzapulumutsidwa pobereka mwana ngati apitiriza
kukhala m'chikhulupiriro, m'chikondi ndi m'kuyera mtima pamodzi ndi
kudzichepetsa konse.

# 3

*Zowayenereza Oyang'anira ndi Atumiki*

1 Mawu woona ndi awa: Ngati munthu akufunitsitsa atakhala
woyang'anira, ndiye kuti akufuna ntchito yabwino. 2 Tsono woyang'anira
ayenera kukhala munthu wopanda chotsutsika nacho, mwamuna wa
mkazi mmodzi yekha, woganiza bwino, wodziretsa, waulemu, wosamala
bwino alendo, wodziwa kuphunzitsa. 3 Asakhale chidakwa, asakhale
wandewu, koma wofatsa, asakhale wokonda mikangano, kapena wokonda
ndalama. 4 Akhale wodziwa kusamala bwino banja lake ndi kulera ana
ake bwino, kuti akhale omvera ndi aulemu weniweni. 5 (Ngati munthu
sadziwa kusamala banja lake lomwe, angathe bwanji kusamala mpingo
wa Mulungu?) 6 Asakhale wongotembenuka mtima kumene kuopa kuti
angadzitukumule napezeka pa chilango monga Satana. 7 Ayeneranso

kukhala munthu wambiri yabwino ndi akunja, kuti anthu asamutonze
nagwa mu msampha wa Satana.
8 Momwemonso atumiki, akhale anthu oyenera ulemu, woona mtima,
osakhala okonda zoledzeretsa, osakonda kupeza zinthu mwachinyengo.
9 Ayenera kugwiritsa mozama choonadi cha chikhulupiriro ndi kukhala
ndi chikumbumtima chabwino. 10 Ayambe ayesedwa kaye, ndipo ngati
palibe kanthu kowatsutsa, aloleni akhale atumiki.
11 Momwemonso, akazi akhale olemekezeka, osasinjirira koma oganiza
bwino ndi odalirika pa chilichonse.
12 Mtumiki akhale wokhulupirika kwa mkazi wake ndipo ayenera
kukhala wosamalira bwino ana ake ndi onse a pa khomo pake. 13 Iwo
amene atumikira bwino amakhala ndi mbiri yabwino ndipo amakhala
chitsimikizo chachikulu cha chikhulupiriro chawo mwa Khristu Yesu.

### *Cholinga cha Malangizo a Paulo*

14 Ngakhale ndili ndi chiyembekezo choti ndifika komweko posached-
wapa, ndikukulemberani malangizo awa. 15 Ine zina zikandichedwetsa
kubwera, mudziwe za mmene anthu ayenera kukhalira m'Nyumba
ya Mulungu, imene ndi mpingo wa Mulungu wamoyo, mzati ndi
maziko achoonadi. 16 Mosakayikira, chinsinsi cha chikhulupiriro chathu
chachikulu:

Khristu anaonekera ali ndi thupi la munthu,
    Mzimu anamuchitira umboni,
angelo anamuona,
    analalikidwa pakati pa mitundu yonse,
dziko lapansi linamukhulupirira,
    anatengedwa kupita kumwamba mwa ulemerero.

# 4

### *Malangizo kwa Timoteyo*

1 Mzimu akunena momveka bwino kuti m'masiku otsiriza anthu ena
adzataya chikhulupiriro chawo ndi kutsatira mizimu yonyenga ndi zinthu
zophunzitsidwa ndi ziwanda. 2 Ziphunzitso zimenezi zimachokera ku
chinyengo cha anthu onama, amene chikumbumtima chawo china-
matidwa ndi chitsulo cha moto. 3 Iwo amaletsa anthu ukwati ndi
kuwalamula kuti asamadye zakudya zina, zimene Mulungu analenga kuti
amene anakhulupirira ndi kudziwa choonadi, azidye moyamika. 4 Pakuti
chilichonse chimene Mulungu analenga ndi chabwino, ndipo chilichonse
chisasalidwe, akamachilandira moyamika, 5 pakuti chimayeretsedwa ndi
mawu a Mulungu ndi pemphero.
6 Ngati abale uwalangiza zimenezi, udzakhala mtumiki wabwino
wa Khristu Yesu, woleredwa m'choonadi cha chikhulupiriro ndi
m'chiphunzitso chabwino chimene wakhala ukutsata. 7 Koma upewe
nkhani zachabe ndi nthano za amayi okalamba; m'malo mwake udzi-
phunzitse kukhala moyo wolemekeza Mulungu. 8 Pakuti kulimbitsa thupi
kumapindulitsapo pang'ono, koma moyo woopa Mulungu umapindulitsa
pa zonse. Umatilonjeza moyo pa moyo uno ndiponso pa moyo umene
ukubwerawo.
9 Amenewa ndi mawu odalirika ndi oyenera kuwalandira kwathunthu.
10 N'chifukwa chake timagwira ntchito molimbika ndi kuyesetsa, chifukwa
tayika chiyembekezo chathu mwa Mulungu wamoyo, amene ndi Mpulu-
mutsi wa anthu onse, koma makamaka wa amene amakhulupirira.

11 Lamulira ndi kuphunzitsa zinthu zimenezi. 12 Usalole kuti wina
akupeputse chifukwa ndiwe wachinyamata, koma khala chitsanzo kwa
okhulupirira pa mayankhulidwe, pa makhalidwe, pa chikondi, pa
chikhulupiriro ndi pa kuyera mtima. 13 Mpaka nditabwera, udzipereke
powerenga mawu a Mulungu kwa anthu, kulalikira ndi kuphunzitsa.
14 Usanyozere mphatso yako yomwe inapatsidwa kwa iwe kudzera
m'mawu auneneri pamene gulu la akulu ampingo linakusanjika manja.

15 Uzichita zimenezi mosamalitsa ndi modzipereka kwathunthu, kuti
aliyense aone kuti ukupita m'tsogolo. 16 Samala kwambiri moyo wako
ndi ziphunzitso zako. Uzichitabe zimenezi chifukwa ukatero, udzadzipu-
lumutsa ndiponso udzapulumutsa okumvetsera.

# 5

*Malangizo kwa Amayi Amasiye, Akulu Ampingo ndi Akapolo*

1 Usadzudzule munthu wachikulire mokalipa, koma umuchenjeze ngati
abambo ako. Achinyamata uwatenge ngati abale ako. 2 Amayi achikulire
uwatenge ngati amayi ako ndipo amayi achitsikana uwatenge ngati alongo
ako, n'kuyera mtima konse.

3 Uziwachitira ulemu akazi amasiye amene ali okhaokha. 4 Koma
ngati mkazi wamasiye ali ndi ana ndi zidzukulu, anawo ayambe
aphunzira kukwaniritsa udindo wawo pa banja lawo moopa Mulungu,
potero akubweza zabwino kwa makolo awo ndi agogo awo. Pakuti
zimenezi ndiye zimakondweretsa Mulungu. 5 Mkazi wamasiye amene
ali yekha ndi wopanda womuthandiza, ameneyo wayika chiyembekezo
chake pa Mulungu, ndipo amapemphera kosalekeza usana ndi usiku
kuti Mulungu azimuthandiza. 6 Koma mkazi wamasiye amene aman-
gokhalira kuchita zosangalatsa moyo wake, wafa kale ngakhale akanali
ndi moyo. 7 Pereka malangizo amenewa kwa anthu kuti akhale opanda
zolakwa. 8 Ngati wina sasamalira abale ake, makamaka a m'banja mwake
mwenimweni, ameneyo wakana chikhulupiriro ndipo ndi woyipa kuposa
wosakhulupirira.

9 Mayi wamasiye aliyense amene sanakwanitse zaka 60 zakubadwa,
asakhale m'gulu la akazi amasiye. Akhale woti anakwatiwapo ndi
mwamuna wake mmodzi yekha. 10 Akhale mayi woti amadziwika
bwino pa ntchito zake zabwino monga kulera ana, kusamalira alendo,
kusambitsa mapazi a anthu a Mulungu, kuthandiza amene ali pa mavuto
ndi kudzipereka pa ntchito zonse zabwino.

11 Akazi amasiye achitsikana, usawayike m'gulu limeneli. Pakuti zilako-
lako zawo zikayamba kuwavutitsa n'kuwalekanitsa ndi Khristu, amafuna
kukwatiwanso. 12 Zikatero amadziweruza okha chifukwa aphwanya
lonjezo lawo loyamba. 13 Komanso amakhala ndi chizolowezi cha ulesi
ndi kumangoyenda khomo ndi khomo. Ndipo sikungokhala aulesi kokha
komanso kuchita miseche, kudududkira za eni ake, kumangokamba zinthu
zosayenera kukamba. 14 Kotero, ndikulangiza akazi amasiye achitsikana
kuti akwatiwe, akhale ndi ana, asamalire makomo awo ndipo asamupatse
mdani mpata wonyoza 15 Akazi amasiye ena apatuka kale n'kumatsatira
Satana.

16 Ngati mayi aliyense wokhulupirira ali ndi akazi amasiye amene
akuwasamalira, apitirizebe kuwasamalira ndipo asalemetse mpingo, kuti
mpingo uthandize akazi amasiye amene ali okhaokha.

17 Akulu ampingo amene amayang'anira bwino zochitika za mu mpingo,
ndi oyenera ulemu wowirikiza, makamaka amene ntchito yawo ndi kula-
likira ndi kuphunzitsa. 18 Pakuti Mawu a Mulungu amati, "Musamange
ng'ombe pakamwa pamene ikupuntha tirigu," ndi "Wantchito ngoyenera
kulandira malipiro ake." 19 Usamamvere mawu oneneza akulu ampingo
pokhapokha patakhala mboni ziwiri kapena zitatu. 20 Akulu ampingo
amene akuchimwa, uwadzudzule poyera kuti ena aphunzirepo.
21 Ndikukulamulira pamaso pa Mulungu, pamaso pa Yesu Khristu ndi
pamaso pa angelo osankhika, kuti usunge malangizowa mosachotsera
ndipo usachite kalikonse mokondera.
22 Usafulumire kusanjika manja munthu, ndipo usavomerezane ndi
anthu ena pa machimo. Usunge bwino kuyera mtima kwako.
23 Uleke kumangomwa madzi okha, koma uzimwako vinyo pang'ono
chifukwa cha vuto lako la m'mimba ndi kudwala kwako kwa pafupipafupi.
24 Anthu ena machimo awo amaonekeratu poyera, amakafika pa
mpando wachiweruzo eni akewo asanakafike. Machimo a anthu ena
amabwera m'mbuyo mwawo. 25 Momwemonso, ntchito zabwino zi-
maonekera poyera, ndipo ngakhale zipande kutero, sizingatheke kubisika.

# 6

1 Onse amene ali mu ukapolo ayenera kuona ambuye awo ngati oyenera
kuwachitira ulemu, kuti anthu anganyoze dzina la Mulungu ndi chi-
phunzitso chathu. 2 Amene ambuye awo ndi okhulupirira, asawapeputse
chifukwa ambuye ndi abale m'chikhulupiriro. M'malo mwake akuyenera
kuwatumikira bwino chifukwa ambuye wawo ndi okondedwa monga
okhulupirira ndiponso ndi odzipereka kusamalira akapolo awo.

### *Aphunzitsi Onyenga ndi Kukonda Ndalama*

Zinthu izi ukuyenera kuziphunzitsa ndi kuwalamula anthu. 3 Ngati wina
aphunzitsa zosiyana ndi zimenezi, wosagwirizana ndi malangizo woona
a Ambuye athu Yesu Khristu ndi chiphunzitso cholemekeza Mulungu,
4 ameneyo ndi wodzitukumula ndipo sakudziwa chilichonse. Iyeyo ali ndi
maganizo oyipa, wokonda kusemphana mawu ndi kutsutsana. Zimenezi
zimabweretsa nsanje, mikangano, m'nyozo, kuganizirana zoyipa, 5 ndi
kulimbana kosatha pakati pa anthu amitima yopotoka amene alandidwa
choonadi ndipo amaganiza kuti kulemekeza Mulungu ndi njira yopezera
chuma.
6 Koma kulemekeza Mulungu kuli ndi phindu lalikulu. 7 Pakuti sitinab-
weretse kanthu m'dziko lapansi, ndipo sitingatengenso kanthu pochoka
m'dziko lapansi. 8 Koma ngati tili ndi chakudya ndi zovala, zimenezi
zitikwanire. 9 Anthu amene amafuna kulemera amagwa m'mayesero
ndi mu msampha ndi m'zilakolako zambiri zopusa ndi zoopsa zimene
zimagwetsera anthu m'chitayiko ndi m'chiwonongeko. 10 Pakuti kukonda
ndalama ndiye muzu wa zoyipa za mitundu yonse. Anthu ena ofunitsitsa
ndalama, asochera ndipo asiya njira yachikhulupiriro ndipo adzitengera
zowawitsa zambiri.

### *Malangizo Otsiriza kwa Timoteyo*

11 Koma iwe, munthu wa Mulungu, thawa zinthu zonsezi. Tsatira
chilungamo, moyo wolemekeza Mulungu, chikhulupiriro, chikondi,
kupirira ndi kufatsa. 12 Menya nkhondo yabwino yachikhulupiriro.
Gwiritsitsa moyo wosatha umene anakuyitanira pamene unavomereza

bwino lomwe pamaso pa mboni zambiri. [13] Ndikukulamula pamaso
pa Mulungu amene amapatsa moyo zinthu zonse, ndiponso pamaso pa
Khristu Yesu amene pochitira umboni pamaso pa Pontiyo Pilato, ananena
zoona zenizeni. [14] Usunge lamuloli mopanda banga ndi cholakwa kufikira
Ambuye athu Yesu Khristu ataonekera. [15] Pa nthawi yake Mulungu
adzamubweretsa kwa ife. Mulungu ndi wodalitsika ndipo Iye yekha ndiye
Wolamulira, Mfumu ya mafumu, Mbuye wa ambuye. [16] Ndiye yekha
wosafa ndipo amakhala m'kuwala koopsa. Mulungu amene munthu
aliyense sanamuone. Kwa Iye kukhale ulemu ndi mphamvu mpaka
muyaya. Ameni.

### *Za Kudalira Chuma*

[17] Anthu onse amene ali ndi chuma uwalamule kuti asanyade kapena
kuyika mitima yawo pa chuma chimene n'chosadalirika. Koma chiyem-
bekezo chawo chikhale mwa Mulungu amene amatipatsa mowolowa-
manja zonse zotisangalatsa. [18] Uwalamule kuti azichita zabwino, kuti
azikhala olemera pa ntchito zabwino, owolowamanja ndi okonda ku-
gawana zinthu zawo ndi anzawo. [19] Potero adzadziwunjikira chuma
chokhalitsa ngati maziko okhazikika a nthawi zakutsogolo, kuti akalandire
moyo, umene ndi moyo weniweni.

### *Mawu Otsiriza*

[20] Timoteyo, samalitsa zimene unapatsidwa. Upewe nkhani zopanda
pake zosalemekeza Mulungu ndiponso maganizo otsutsana amene ama-
ganizidwa molakwika kuti ndi nzeru. [21] Anthu ena chifukwa chovomereza
nzeru zotere, asochera n'kutaya chikhulupiriro chawo.
Chisomo chikhale nawe.

# KALATA YACHIWIRI YA PAULO YOLEMBERA TIMOTEYO

1 Paulo mtumwi wa Khristu Yesu mwa chifuniro cha Mulungu. Anandi-
tuma kuti ndilalike za lonjezo la moyo umene uli mwa Khristu Yesu.
2 Kwa Timoteyo, mwana wanga wokondedwa:
Chisomo, chifundo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate ndi
Ambuye athu Yesu Khristu.

### *Chilimbikitso Pokhala Wokhulupirika*

3 Ndikuyamika Mulungu amene ndimamutumikira ndi chikum-
bumtima chosatsutsika, monga momwe ankachitira makolo anga.
Usiku ndi usana ndimakukumbukira mosalekeza m'mapemphero anga.
4 Ndikamakumbukira misozi yako, ndimalakalaka nditakuona kuti
ndidzazidwe ndi chimwemwe. 5 Ndakumbukira za chikhulupiriro chako
choona chimene chinayamba mwa agogo ako a Loisi ndi mwa amayi ako
Yunike ndipo ndikutsimikiza mtima kuti chilinso mwa iwe.

### *Kumvera Paulo ndi Uthenga Wabwino*

6 N'chifukwa chake ndikukukumbutsa kuti upemerere monga amachi-
tira moto, mphatso imene Mulungu anakupatsa nditakusanjika manja.
7 Pakuti Mzimu amene Mulungu anatipatsa, si Mzimu wotipatsa manyazi,
koma Mzimu wotipatsa mphamvu, chikondi ndi kudzisunga.
8 Choncho usachite manyazi kuchitira umboni Ambuye athu, kapena
kuchita manyazi chifukwa cha ine wam'ndende. Koma umve nane
zowawa chifukwa cha Uthenga Wabwino, mothandizidwa ndi mphamvu
za Mulungu. 9 Iye anatipulumutsa ndipo anatiyitanira ku moyo oyera
mtima, osati chifukwa cha chilichonse chimene tinachita, koma chifukwa
cha chikonzero ndi chisomo chake. Chisomo chimenechi anatipatsa ife
mwa Khristu Yesu nthawi isanayambe. 10 Koma tsopano Mulungu watiwu-
lulira kudzera m'kuoneka kwa Mpulumutsi wathu, Khristu Yesu, amene
anathetsa mphamvu za imfa ndipo mwa Uthenga Wabwino anaonetsa
poyera moyo umene sungafe. 11 Ine ndinasankhidwa kukhala wamthenga,
ndi mtumwi ndi mphunzitsi wa Uthenga Wabwinowu. 12 N'chifukwa
chake ndikuvutika monga ndililimu. Komabe zimenezi sizikundichititsa
manyazi, popeza ndikumudziwa amene ndamukhulupirira ndipo ndikut-
simikiza mtima kuti akhoza kusamalira chimene ndinamusungitsa mpaka
tsiku lijalo.
13 Zimene unamva kwa ine, uzisunge kuti zikhale chitsanzo cha
chiphunzitso choona, mwa chikhulupiriro ndi chikondi mwa Khristu
Yesu. 14 Samalira bwino zokoma zimene anakusungitsa. Uzisamalire
mothandizidwa ndi Mzimu Woyera amene amakhala mwa ife.

### *Zitsanzo za Kusakhulupirika ndi Kukhulupirika*

15 Iwe udziwa kuti onse a m'chigawo cha Asiya ananandithawa, kuphatik-
izapo Fugelo ndi Herimogene omwe.
16 Mulungu achitire chifundo banja lonse la Onesiforo chifukwa
ankandisangalatsa kawirikawiri ndipo sankachita nane manyazi ngakhale
ndinali womangidwa ndi maunyolo. 17 M'malo mwake, atangofika ku
Roma, anandifunafuna ndipo anandipeza. 18 Ambuye amulole kuti

adzalandire chifundo kwa Ambuye pa tsiku lijalo! Ukudziwa bwino
momwe iye ananandithandizira m'njira zosiyanasiyana ku Efeso.

# 2

1 Tsono iwe, mwana wanga, limbika m'chisomo chimene chili mwa
Khristu Yesu. 2 Ndipo zinthu zimene unamva ine ndikuziyankhula
pamaso pa mboni zambiri, uziphunzitse kwa anthu odalirika amene
akaphunzitsenso ena. 3 Umve nane zowawa, monga msilikali wa
Khristu Yesu. 4 Palibe msilikali amene ali pa ntchito amagwiranso
ntchito za anthu wamba, iye amafuna kukondweretsa bwana wolamulira.
5 Chimodzimodzinso, munthu amene ali pa mpikisano waliwiro, salandira
mphotho ya wopambana pokhapokha atatsiriza monga mwa malamulo a
mpikisanowo. 6 Mlimi wolimbika ndi amene amayembekezereka kukhala
woyambirira kulandira gawo la zokolola. 7 Lingalira zimene ndikunenazi,
pakuti Ambuye adzakuzindikiritsa zonsezi.

8 Kumbukira Yesu Khristu wochokera ku mtundu wa Davide kuti anauka
kwa akufa. Uwu ndiye uthenga wanga wabwino 9 umene ndikuwuvutikira
choterewu mpaka kumangidwa ndi maunyolo ngati wakuba. Koma
mawu a Mulungu sanamangidwe ndi maunyolo. 10 Choncho ndikupirira
chilichonse chifukwa cha osankhidwa, kuti nawonso apulumutsidwe ndi
Khristu Yesu ndi kulandira ulemerero wosatha.

11 Mawu oyenera kuwadalira ndi awa:

Ngati ife tinafa naye pamodzi,
tidzakhalanso moyo pamodzi naye.

12 Ngati tinapirira,
tidzalamuliranso naye pamodzi.

Ngati ife timukana,
Iye adzatikananso.

13 Ngati ndife osakhulupirika,
Iye adzakhalabe wokhulupirika
popeza sangathe kudzikana.

### *Kuthana ndi Aphunzitsi Onyenga*

14 Uziwakumbutsa anthu a Mulungu zinthu izi. Uwachenjeze pamaso
pa Mulungu kuti asamakangane pa za mawu. Zimenezi n'zopanda
phindu ndipo zimangowononga amene akumvawo. 15 Uyesetse kukhala
wovomerezeka pamaso pa Mulungu monga wantchito wopanda chifukwa
chochitira manyazi amene amalalikira mawu achoonadi molondola.
16 Upewe nkhani zopanda pake, zosalemekeza Mulungu, chifukwa anthu
oyankhula zotere amanka napotokerapotokera. 17 Chiphunzitso chawo
chidzafalikira ngati chilonda. Mwa anthuwa muli Humenayo ndi Fileto.
18 Iwowa apatuka pa choonadi. Iwo amaphunzitsa kuti kuuka kwa
akufa kunachitika kale, motero amawononga chikhulupiriro cha anthu
ena. 19 Komabe maziko olimba, amene Mulungu anawayika ngokhazikika,
ndipo mawu olembedwapo ndi awa: "Yehova amadziwa amene ndi
ake," ndiponso, "Aliyense amene amavomereza dzina la Ambuye ayenera
kusiya zoyipa."

20 M'nyumba yayikulu simukhala ziwiya zagolide ndi zasiliva zokha,
koma mumakhalanso zamtengo ndi zadothi. Zina zimakhala za ntchito
yapamwamba, zina za ntchito wamba. 21 Munthu akadziyeretsa n'kusiya

ntchito za wambazi, adzakhala chiwiya cha ntchito yapamwamba, woy-
eretsedwa, ndi waphindu kwa Ambuye wake, wokonzeka kugwira ntchito
iliyonse yabwino.
22 Thawa zilakolako zoyipa zachinyamata. Funafuna chilungamo,
chikhulupiriro, chikondi ndi mtendere pamodzi ndi amene akuyitanira
pa dzina la Ambuye ndi mtima osadetsedwa. 23 Ukane matsutsano oyipa
ndi opusa, chifukwa amayambitsa mikangano. 24 Ndiponso mtumiki
wa Ambuye asamakangane ndi anthu, koma azikhala wachifundo kwa
aliyense, wodziwa kuphunzitsa, osati wokalipakalipa. 25 Otsutsana naye
awalangize mofatsa, mwina Mulungu adzawapatsa mwayi woti asinthike
ndi kuzindikira choonadi. 26 Motero nzeru zawo zidzabweramo, ndipo
adzathawa msampha wa mdierekezi, amene anawagwira ukapolo kuti
azichita zofuna zake.

# 3

### *Zoopsa za M'masiku Otsiriza*

1 Koma dziwa izi: M'masiku otsiriza kudzafika nthawi zoopsa kwambiri.
2 Anthu adzakhala odzikonda, okonda ndalama, odzitama, onyada,
achipongwe, osamvera makolo awo, osayamika, wopanda chiyero.
3 Adzakhala wopanda chikondi, osakhululuka, osinjirira, osadziletsa,
ankhanza, osakonda zabwino, 4 opereka anzawo kwa adani awo, osaopa
zoyipa, odzitukumula, okonda zowasangalatsa m'malo mokonda Mu-
lungu. 5 Adzakhala ndi maonekedwe achipembedzo koma mphamvu yake
ndi kumayikana. Anthu amenewa uziwapewa.
6 Iwowa ndi anthu aja amene amayendayenda m'makomo a
anthu n'kumanyenga akazi ofowoka m'maganizo, olemedwa ndi
machimo ndiponso otengeka ndi zilakolako zoyipa zamitundumitundu,
7 amaphunzira nthawi zonse koma samatha kuzindikira choonadi.
8 Monga momwe Yanesi ndi Yambere anawukira Mose, momwemonso
anthu amenewa amawukira choonadi. Nzeru zawo ndi zowonongeka
ndipo pa za chikhulupiriro, ndi okanidwa. 9 Koma sadzapita nazo patali
kwambiri zimenezi, pakuti anthu onse adzaona kupusa kwawo monga
anachitira Yanesi ndi Yambere.

### *Paulo Alimbikitsa Timoteyo*

10 Tsono iwe, umadziwa zonse zimene ndimaphunzitsa, makhalidwe
anga, cholinga changa, chikhulupiriro changa, kuleza mtima kwanga,
chikondi changa, ndi kupirira kwanga, 11 mazunzo anga, masautso
anga, monga zinandichitikira ku Antiokeya, ku Ikoniya ndi ku Lusi-
tra. Ndinazunzika kwambiri. Koma Ambuye anandipulumutsa pa
zonsezi. 12 Kunena zoona, munthu aliyense amene akufuna kukhala
moyo wolemekeza Mulungu mwa Khristu Yesu, adzazunzikadi, 13 pomwe
anthu oyipa ndi onyenga adzanka nayipirayipira, kunamiza ena, iwo
n'kumanamizidwanso. 14 Koma iwe pitiriza zimene waziphunzira ndi
kuzivomereza, chifukwa ukudziwa amene anakuphunzitsa zimenezi.
15 Kuyambira uli wamng'ono wakhala ukudziwa Malemba Oyera, amene
akhoza kukupatsa nzeru zokupulumutsa kudzera m'chikhulupiriro cha
mwa Yesu Khristu. 16 Malemba onse anawalembetsa ndi Mulungu, ndipo
othandiza pophunzitsa, podzudzula, pokonza cholakwika ndi polangiza
za chilungamo 17 kuti munthu wa Mulungu akonzekere bwino lomwe
kugwira ntchito iliyonse yabwino.

# 4

1 Pamaso pa Mulungu ndi pamaso pa Khristu Yesu, amene adza-
weruza amoyo ndi akufa omwe pamene adzaonekera ndi ufumu wake,
ndikukulamula kuti: 2 Lalikira Mawu; khala wokonzeka pa nthawi yake,
ngakhale pamene si pa nthawi yake. Konza zolakwa zawo, dzudzula
ndipo limbikitsa moleza mtima kwambiri ndi malangizo osamalitsa.
3 Pakuti idzafika nthawi imene anthu adzakana chiphunzitso choona.
M'malo mwake, chifukwa chokhumba kumva zowakomera zokha, adza-
sonkhanitsa aphunzitsi ambiri omawawuza zimene iwo akufuna kumva.
4 Sadzafuna kumva choona koma adzafuna kumva nthano chabe. 5 Koma
iwe, khala tcheru nthawi zonse, pirira m'zovuta, gwira ntchito ya mlaliki,
gwira ntchito zonse za utumiki wako.
6 Pakuti moyo wanga wayamba kale kuthiridwa ngati nsembe,
ndipo nthawi yakwana yoti ndinyamuke ulendo wanga. 7 Ndamenya
nkhondo yabwino, ndatsiriza bwino mpikisano wa liwiro ndipo ndasunga
chikhulupiriro. 8 Tsopano mphotho yanga ikundidikira imene ndi chipewa
cha chilungamo, imene Ambuye, woweruza wolungama, adzandipatsa pa
tsiku lijalo, osati ine ndekha komanso onse amene akufunitsitsa kubwera
kwake.

### *Ndemanga ya Paulo*

9 Uyesetse kubwera kuno msanga. 10 Paja Dema anandisiya chifukwa
chokonda dziko lapansi lino, ndipo anapita ku Tesalonika. Kresike
anapita ku Galatiya ndipo Tito anapita ku Dalimatiya. 11 Ndatsala ndi
Luka yekha basi. Mutenge Marko ndipo ubwere naye kuno, chifukwa
amandithandiza mu utumiki wanga. 12 Ndatumiza Tukiko ku Efeso.
13 Pobwera, unditengere chofunda pamwamba chimene ndinachisiya
kwa Kupro ku Trowa. Unditengerenso mabuku anga, makamaka aja
azikopawa.
14 Alekisandro, mmisiri wa zitsulo anandichitira zoyipa kwambiri.
Ambuye adzamubwezera pa zimene anachita. 15 Iwenso ukhale naye
tcheru chifukwa anatsutsa kwambiri uthenga wathu.
16 Podziteteza koyamba pa mlandu wanga, panalibe ndi mmodzi yemwe
amene anandithandiza, koma aliyense anandithawa. Mulungu awakhu-
lulukire. 17 Koma Ambuye anayima nane limodzi, ndipo anandipatsa
mphamvu, kuti kudzera mwa ine, uthenga ulalikidwe kwambiri, ndikuti
anthu a mitundu ina amve. Ndipo ndinalanditsidwa m'kamwa mwa
mkango. 18 Ambuye adzandilanditsa ku chilichonse chofuna kundichita
choyipa ndipo adzandisamalira bwino mpaka kundilowetsa chonse mu
ufumu wake wakumwamba. Kwa Iye kukhale ulemerero mpaka muyaya.

### *Mawu Otsiriza*

19 Pereka moni kwa Prisila ndi Akura pamodzi ndi banja lonse la
Onesiforo. 20 Erasto anatsalira ku Korinto. Trofimo ndinamusiya
akudwala ku Mileto. 21 Uyesetse kubwera kuno nthawi yozizira isanafike.
Eubulo akupereka moni, ndiponso Pude, Lino, Klaudiya ndi abale onse
nawonso akupereka moni.
22 Ambuye akhale ndi mzimu wako. Chisomo chikhale ndi inu nonse.

# KALATA YA PAULO YOLEMBERA TITO

[1] Ndine Paulo, mtumiki wa Mulungu, ndi mtumwi wa Yesu Khristu. Ndinatumidwa kuti nditsogolere amene Mulungu anawasankha ku chikhulupiriro ndi ku chidziwitso cha choonadi chimene chimawafikitsa
ku moyo wolemekeza Mulungu [2] ndi kuwapatsa chiyembekezo cha moyo wosatha, umene Mulungu amene sanama, analonjeza nthawi isanayambe.
[3] Pa nthawi yake Mulungu, Mpulumutsi wathu anawulula poyera mawu ake ndipo analamula kuti ndipatsidwe udindo wolalikira uthengawu.
[4] Kwa Tito, mwana wanga weniweni m'chikhulupiriro cha ife tonse:

Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate ndi Khristu Yesu Mpulumutsi wathu.

### *Ntchito ya Tito ku Krete*

[5] Ndinakusiya ku Krete kuti ulongosole zonse zimene ndinazisiya zisanathe ndiponso usankhe akulu ampingo m'mizinda yonse, monga
momwe ndinakulamulira. [6] Mkulu wampingo akhale munthu wopanda cholakwa, akhale wa mkazi mmodzi yekha, munthu amene ana ake ndi
okhulupirira, osati amakhalidwe oyipa ndi osamvera. [7] Popeza mkulu wa mpingo amayendetsa ntchito za banja la Mulungu, ayenera kukhala wopanda cholakwa, asakhale womva zayekha, kapena wopsa mtima msanga, kapena womwa zoledzeretsa, kapena wandewu, kapena wopeza
phindu mwachinyengo. [8] Koma akhale wosamala bwino alendo, wokonda zabwino, wodziretsa, wolungama, woyera mtima ndi wosunga mwambo.
[9] Iye ayenera kugwiritsa mawu okhulupirika monga tinaphunzitsira, kuti athe kulimbikitsa ena ndi chiphunzitso choona ndiponso kugonjetsa amene atsutsana nacho.

### *Kudzudzula Olephera Kuchita Bwino*

[10] Paja pali anthu ambiri osaweruzika, makamaka m'gulu la anthu a mdulidwe, oyankhula nkhani zopanda pake ndi kusocheretsa an-
zawo. [11] Ayenera kuletsedwa kuyankhula chifukwa akusokoneza mabanja athunthu pophunzitsa zinthu zomwe sayenera kuwaphunzitsa. Iwo
amachita izi kuti apeze ndalama mwachinyengo. [12] Mneneri wina, mmodzi wa iwo omwewo anati, "Akrete nthawi zonse ndi amabodza,
akhalidwe loyipitsitsa ndiponso alesi adyera." [13] Mawu amenewa ndi woona. N'chifukwa chake, uwadzudzule mwamphamvu, kuti akhale
ndi chikhulupiriro choona, [14] kuti asasamalenso nthano za Chiyuda, ndi
malamulo a anthu amene akukana choonadi. [15] Kwa oyera mtima, zinthu zonse ndi zoyera, koma kwa amene ndi odetsedwa ndi osakhulupirira, palibe kanthu koyera. Kunena zoona, mitima yawo ndi chikumbumtima
chawo, zonse n'zodetsedwa. [16] Iwo amati amadziwa Mulungu, pamene ndi zochita zawo amamukana. Ndi anthu onyansa ndi osamvera, ndi osayenera kuchita kalikonse kabwino.

## 2

### *Malangizo Osiyanasiyana*

1 Koma iwe uziphunzitsa zogwirizana ndi chiphunzitso choona.
2 Phunzitsa amuna achikulire kuti akhale osaledzera, aulemu wawo,
odziletsa, okhwima m'chikhulupiriro, m'chikondi ndi m'kupirira.

3 Chimodzimodzinso, phunzitsa amayi achikulire kuti akhale aulemu
m'makhalidwe awo, asakhale osinjirira anzawo kapena zidakwa, koma
akhale alangizi abwino. 4 Tsono atha kulangiza amayi achichepere
kukonda amuna awo ndi ana awo. 5 Kuwaphunzitsa kukhala odziletsa ndi
oyera mtima, osamala bwino mabanja awo, okoma mtima, ndi ogonjera
amuna awo. Choncho palibe amene adzanyoze mawu a Mulungu.

6 Momwemonso, uwalimbikitse amuna achichepere kuti akhale
odziletsa. 7 Pa zonse iwe mwini ukhale chitsanzo pa ntchito zabwino.
Pa chiphunzitso chako uwonetsa kuona mtima ndi kutsimikiza mtima
kwako. 8 Phunzitsa choonadi kuti anthu asapeze chokutsutsa, motero
wotsutsana nawe adzachita manyazi chifukwa adzasowa kanthu koyipa
kuti atinenere.

9 Phunzitsa akapolo kuti azigonjera ambuye awo mu zinthu zonse ndi
kuwakondweretsa. Asamatsutsane nawo 10 kapena kumawabera, koma
adzionetse kuti ndi odalirika, motero pa zochita zawo zonse adzaonetsa
ubwino wa chiphunzitso cha Mulungu, Mpulumutsi wathu.

11 Pakuti chisomo cha Mulungu chimene chimapulumutsa chaonekera
kwa anthu onse. 12 Chisomo chimatiphunzitsa kukana moyo osalemekeza
Mulungu komanso zilakolako za dziko lapansi. Ndipo chimatiphunzitsa
kukhala moyo odziletsa, olungama ndi opembedza Mulungu nthawi ino,
13 pamene tikudikira chiyembekezo chodala; kuonekera kwa ulemerero
wa Mulungu wathu wamkulu ndi Mpulumutsi, Yesu Khristu, 14 amene
anadzipereka yekha chifukwa cha ife kutiwombola ku zoyipa zonse
ndi kudziyeretsera yekha anthu amene ndi akeake, achangu pa ntchito
yabwino.

15 Tsono zimenezi ndi zinthu zomwe uyenera kuphunzitsa. Uziwalim-
bikitsa anthu ndi kuwatsutsa komwe. Uzichita zimenezi ndi ulamuliro
wonse. Wina aliyense asakupeputse ayi.

# 3

*Kuchita Ntchito Zabwino*

1 Uwakumbutse anthu kuti azigonjera oweruza ndi olamulira,
aziwamvera ndi kukhala okonzeka kuchita chilichonse chabwino.
2 Asamachitire chipongwe aliyense, asamakangane, akhale ofatsa ndipo
oganizira ena, ndipo nthawi zonse akhale aulemu kwa anthu onse.

3 Nthawi ina tinali opusa, osamvera, onamizidwa ndi omangidwa ndi
zilakolako ndi zokondweretsa zamitundumitundu. Tinkakhala moyo wad-
umbo ndi wakaduka, odedwa ndiponso odana wina ndi mnzake. 4 Koma
kukoma mtima ndi chikondi cha Mulungu Mpulumutsi wathu chitaonek-
era, 5 Iye anatipulumutsa, osati chifukwa cha ntchito zathu zolungama
zimene tinachita koma chifukwa cha chifundo chake. Anatipulumutsa
potisambitsa, kutibadwitsa kwatsopano ndi kutikonzanso mwa Mzimu
Woyera 6 amene anatipatsa mowolowamanja kudzera mwa Yesu Khristu
Mpulumutsi wathu, 7 kuti titalungamitsidwa mwachisomo chake, tikhale
olowam'malo okhala ndi chiyembekezo cha moyo wosatha. 8 Mawuwa
ndi okhulupirika ndipo ine ndikufuna kuti iwe utsindike zinthu izi, kuti
amene akhulupirira Mulungu adzipereke kuchita ntchito zabwino. Zinthu
izi ndi zabwino kwambiri ndi zopindulitsa kwa aliyense.

9 Koma upewe kufufuzafufuza zopusa, kuwerengawerenga mndan-
danda wa mibado ya makolo, mikangano ndi mitsutso pa za Malamulo,
chifukwa zimenezi ndi zosapindulitsa ndi zopanda pake. 10 Munthu
woyambitsa mipatuko umuchenjeze koyamba, ndiponso umuchenjeze
kachiwiri. Kenaka umupewe. 11 Iwe udziwe kuti munthu wotero
ngosokoneza ndi wochimwa, ndipo akudzitsutsa yekha.

*Mawu Otsiriza*

12 Ndikadzamutuma Artema kapena Tukiko kwanuko, udzayesetse
kundipeza ku Nikapoli, chifukwa ndatsimikiza kukhala kumeneko pa
nthawi yozizira. 13 Uyesetse chilichonse ungathe kuthandiza Zena
katswiri wa malamulo ndi Apolo, kuti apitirize ulendo wawo, ndipo
uwonetsetse asasowe kanthu. 14 Anthu athu aphunzire kudzipereka
pogwira ntchito zabwino, n'cholinga chakuti athandize zinthu zimene
zikufunika msangamsanga. Ndipo asakhale moyo osapindulitsa.
15 Onse amene ali ndi ine akupereka moni. Upereke moni kwa amene
amatikonda ife m'chikhulupiriro.
Chisomo chikhale ndi inu nonse.

# KALATA YA PAULO YOLEMBERA FILEMONI

1 Kuchokera kwa Paulo, amene ndili m'ndende chifukwa cha Khristu
Yesu ndi Timoteyo m'bale wathu.
Kulembera Filemoni, bwenzi lathu lokondedwa ndi mtumiki mnzathu.
2 Kwa Apiya mlongo wathu, Arkipo msilikali mnzathu, ndiponso mpingo
umene umasonkhana m'nyumba mwanu.
3 Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate athu ndi Ambuye
Yesu Khristu zikhale ndi inu.

*Kuyamika ndi Pemphero*

4 Ine ndimayamika Mulungu wanga nthawi zonse ndikakukumbukira
iwe m'mapemphero anga. 5 Pakuti ndamva za chikondi chako, za
chikhulupiriro chako mwa Ambuye Yesu ndiponso za chikondi chako pa
oyera mtima onse. 6 Ine ndikupemphera kuti mgwirizano wako ndi ife
m'chikhulupiriro ukhale opindulitsa pozamitsa nzeru zako zozindikira
zinthu zilizonse zabwino zimene timagawana chifukwa cha Khristu.
7 M'bale, chikondi chako chandipatsa chimwemwe chachikulu ndi chilim-
bikitso, chifukwa umatsitsimutsa mitima ya anthu a Ambuye.

*Paulo Apempha kuti Amuchitire Chifundo Onesimo*

8 Tsopano ngakhale kuti mwa Khristu ndi tha kulimba mtima ndi
kulamulira kuti uchite zimene uyenera kuchita, 9 komabe ndikupempha
mwachikondi. Ine Paulo, munthu wokalamba, ndipo tsopano ndili
m'ndende chifukwa cha Khristu Yesu, 10 ndikukupempha chifukwa cha
mwana wanga Onesimo, amene ndamubala ndili mu unyolo. 11 Anali
wopanda phindu kwa iwe, koma tsopano wasanduka wa phindu kwa iwe
ndi kwa inenso.
12 Ine ndikumutumizanso kwa iwe tsopano, koma potero ndikukhala
ngati ndikutumiza mtima wanga weniweni. 13 Ndikanakonda
ndikanakhala naye kuno kuti iyeyo azinditumikira m'malo mwako
pamene ndili mu unyolo chifukwa cha Uthenga Wabwino. 14 Koma
sindikufuna kuchita kanthu osakufunsa, n'cholinga chakuti chilichonse
chabwino ungandichitire chikhale mwakufuna kwako osati mokakamiza.
15 Mwina chifukwa chimene unasiyana naye kwa kanthawi ndi chakuti
ukhale nayenso nthawi zonse. 16 Osati ngati kapolo, koma woposa kapolo,
ngati m'bale wokondedwa. Iyeyu ndi wokondedwa kwambiri kwa ine
koma kwa iweyo ndi wokondedwa koposa, ngati munthu komanso ngati
m'bale mwa Ambuye.
17 Tsono ngati umati ndine mnzako, umulandire iyeyu monga momwe
ukanandilandirira ineyo. 18 Ngati anakulakwira kapena kukongola kanthu
kalikonse, ndidzalipira ineyo. 19 Ine, Paulo ndikulemba zimenezi ndi
dzanja langa. Ine ndidzalipira. N'kosafunika kukukumbutsa kuti iweyo
ngongole yako kwa ine ndi moyo wakowo. 20 M'bale, ndikufuna kuti
ndipindule nawe mwa Ambuye; tsono tsitsimutsa mtima wanga mwa
Khristu. 21 Ine ndili ndi chitsimikizo cha kumvera kwako pamene
ndikukulembera kalatayi. Ndikulemba ndikudziwa kuti udzachita
ngakhale kuposa zimene ndakupemphazi.

22 Chinthu chinanso ndi ichi: undikonzere malo, chifukwa
ndikukhulupirira kuti Mulungu adzamvera mapemphero anu ndi
kundibwezera kwa inu.

### *Mawu Otsiriza*

23 Epafra, wam'ndende mnzanga chifukwa cha Khristu Yesu akupereka
moni. 24 Atumiki anzanga awa, Marko, Aristariko, Dema ndi Luka,
akuperekanso moni.
25 Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu chikhale ndi mzimu wako.

# KALATA YOLEMBERA AHEBRI

*Khristu Mwana wa Mulungu Aposa Angelo*

1 Kale lija Mulungu ankayankhula ndi makolo athu pa nthawi
zosiyanasiyana ndiponso mwa njira zosiyanasiyana kudzera mwa aneneri.
2 Koma masiku otsiriza ano, Mulungu wayankhula nafe kudzera mwa
Mwana wake. Mwanayu anamusankha kuti akhale mwini wa zinthu
zonse, ndiponso Mulungu analenga dziko lonse kudzera mwa Iye.
3 Mwanayo ndiye kuwala kwa ulemerero wa Mulungu, chithunzithunzi
chenicheni cha khalidwe lake. Iyeyu amachirikiza zinthu zonse ndi
mphamvu ya mawu ake. Iye atayeretsa anthu kuchoka ku machimo awo,
anakhala pansi kumwamba kudzanja lamanja la Mulungu waulemerero.
4 Mwanayu ndi wamkulu koposa angelo, monga momwe dzina limene
analandira limaposa dzina la angelo.

5 Kodi ndi kwa mngelo uti, kumene Mulungu anati,

"Iwe ndiwe mwana wanga;
Ine lero ndakhala Atate ako."

Kapena kunenanso kuti,

"Ine ndidzakhala abambo ake;
iye adzakhala mwana wanga."

6 Pamene Mulungu amatuma Mwana wake woyamba kubadwa ku dziko
lapansi anati,

"Angelo onse a Mulungu amupembedze Iye."

7 Iye ponena za angelo akuti,

"Mulungu amasandutsa angelo ake mphepo,
amasandutsa atumiki ake malawi amoto."

8 Koma za Mwana wake akuti,

"Inu Mulungu, mpando wanu waufumu udzakhala mpaka muyaya,
ndipo mudzaweruza molungama mu ufumu wanu.

9 Mwakonda chilungamo ndi kudana ndi zoyipa;
N'chifukwa chake, Mulungu wanu wakukwezani kuposa anzanu
pokudzozani mafuta osonyeza chimwemwe."

10 Mulungu akutinso,

"Ambuye, pachiyambi Inu munayika maziko a dziko lapansi;
ndipo zakumwambako ndi ntchito za manja anu.

11 Zimenezi zidzatha, koma Inu ndinu wachikhalire.
Izo zidzatha ngati zovala.

12 Mudzazipindapinda ngati chofunda;
ndipo zidzasinthidwa ngati chovala.
Koma Inu simudzasintha,
ndipo zaka zanu sizidzatha."

13 Kodi ndi kwa Mngelo uti kumene Mulungu ananenapo kuti,

"Khala kudzanja langa lamanja
mpaka nditapanga adani ako
kukhale chopondapo mapazi ako."

14 Kodi angelo onse si mizimu yotumikira odzalandira chipulumutso?

# 2

### *Kusamalira Chipulumutso*

1 N'chifukwa chake, ife tiyenera kusamalira kwambiri zimene tinamva,
kuopa kuti pang'ono ndi pang'ono tingazitaye. 2 Popeza uthenga umene
unayankhulidwa kudzera mwa angelo unali okhazikika ndithu, choncho
aliyense amene ananyozera ndi kusamvera analandira chilango choyen-
era. 3 Nanga ife tidzapulumuka bwanji tikapanda kusamala chipulumutso
chachikulu chotere? Ambuye ndiye anayamba kuyankhula za chipulumut-
sochi, kenaka amenenso anamvawo anatitsimikizira. 4 Mulungu anachi-
tiranso umboni pochita zizindikiro, zinthu zodabwitsa ndi zamphamvu
zamitundumitundu ndi powapatsa mphatso za Mzimu Woyera monga
mwachifuniro chake.

### *Yesu Wofanana ndi Abale ake*

5 Mulungu sanapereke kwa angelo ulamuliro wa dziko limene likubw-
erali, limene ife tikulinena. 6 Koma palipo pena pamene wina anachitira
umboni kuti,

"Kodi munthu ndani kuti muzimukumbukira,
kapena mwana wa munthu kuti muzimusamalira?
7 Munamuchepetsa pang'ono kusiyana ndi angelo;
munamupatsa ulemerero ndi ulemu.
8 Munamupatsa ulamuliro pa zinthu zonse."

Poyika zinthu zonse pansi pa ulamuliro wake, Mulungu sanasiye kanthu
kamene sikali mu ulamuliro wake. Koma nthawi ino sitikuona zinthu
pansi pa ulamuliro wake. 9 Koma tikuona Yesu, amene kwa kanthawi
kochepa anamuchepetsa pang'ono kwa angelo, koma tsopano wavala ule-
merero ndi ulemu chifukwa anamva zowawa za imfa, kuti mwachisomo
cha Mulungu, Iye afere anthu onse.

10 Mulungu amene analenga zinthu zonse ndipo zinthu zonse zilipo
chifukwa cha Iye ndi mwa Iye, anachiona choyenera kubweretsa ana
ake ambiri mu ulemerero. Kunali koyenera kudzera m'njira ya zowawa,
kumusandutsa Yesu mtsogoleri wangwiro, woyenera kubweretsa chipu-
lumutso chawo. 11 Popeza iye amene ayeretsa ndi oyeresedwa onse ndi
abanja limodzi. N'chifukwa chake Yesu sachita manyazi kuwatcha iwo
abale ake. 12 Iye akuti,

"Ine ndidzawuza abale anga za dzina lanu.
Ndidzakuyimbirani nyimbo zamatamando pamaso pa mpingo."
13 Ndiponso,
"Ine ndidzakhulupirira Iyeyo."
Ndiponso Iye akuti,
"Ine ndili pano pamodzi ndi ana amene Mulungu wandipatsa."

14 Tsono popeza kuti anawo ndi anthu, okhala ndi mnofu ndi magazi,
Yesu nayenso anakhala munthu ngati iwowo kuti kudzera mu imfa yake
awononge Satana amene ali ndi mphamvu yodzetsa imfa. 15 Pakuti
ndi njira yokhayi imene Iye angamasule amene pa moyo wawo wonse
anali ngati akapolo chifukwa choopa imfa. 16 Pakuti tikudziwanso kuti
sathandiza angelo, koma zidzukulu za Abrahamu. 17 Chifukwa cha
zimenezi, Iye anayenera kukhala wofanana ndi abale ake pa zonse, kuti
akhale mkulu wa ansembe wachifundo ndi wokhulupirika potumikira
Mulungu, kuti potero achotse machimo a anthu. 18 Popeza Iye mwini

anamva zowawa pamene anayesedwa, Iyeyo angathe kuthandiza amene akuyesedwanso.

# 3

### *Yesu ndi Wamkulu Kuposa Mose*

1 N'chifukwa chake abale oyera mtima, amenenso munayitanidwa
ndi kumwamba, lingalirani za Yesu amene ndi Mtumwi ndi Mkulu
wa ansembe wa chikhulupiriro chimene timavomereza. 2 Iye anali
wokhulupirika kwa Mulungu amene anamupatsa udindowo, monga
momwe Mose anali wokhulupirika m'nyumba yonse ya Mulungu. 3 Yesu
anapezeka woyenera kulandira ulemu waukulu kuposa Mose, monga
momwemonso womanga nyumba amalandira ulemu waukulu kuposa
nyumbayo. 4 Pakuti nyumba iliyonse imamangidwa ndi munthu wina,
koma amene anapanga zonse ndi Mulungu. 5 Mose anali wokhulupirika
monga mtumiki m'nyumba yonse ya Mulungu, kuchitira umboni zimene
zidzayankhulidwe m'tsogolo. 6 Koma Khristu ndi wokhulupirika monga
mwana pa nyumba ya Mulungu. Ndipo ndife nyumba yake ngati tipitirire kulimbika mtima ndi kunyadira zomwe tikuyembekerazo.

### *Chenjezo pa Kusakhulupirira*

7 Tsono monga Mzimu Woyera akuti,
"Lero mukamva mawu ake,
8 musawumitse mitima yanu
ngati munachitira pamene munawukira,
pa nthawi yoyesedwa m'chipululu.
9 Pamene makolo anu anandiputa ndi kundiyesa,
ndipo kwa zaka makumi anayi anaona zimene Ine ndinachita.
10 N'chifukwa chake ndinawukwiyira m'badowo,
ndipo Ine ndinati, 'Nthawi zonse mitima yawo imasochera,
ndipo iwo sadziwa njira zanga.'
11 Kotero Ine ndinalumbira nditakwiya kuti,
'Iwo sadzalowa mu mpumulo wanga.' "

12 Abale samalani, kuti pasapezeke wina aliyense mwa inu wokhala
ndi mtima woyipa ndi wosakhulupirira, womulekanitsa ndi Mulungu
wamoyo. 13 Koma muzilimbikitsana tsiku ndi tsiku, ikanalipo nthawi
imene imatchedwa kuti "Lero" kuti aliyense wa inu mtima wake usawumitsidwe ndi chinyengo cha tchimo. 14 Pakuti timakhala anzake a
Khristu, ngati tigwiritsitsa mpaka potsiriza chitsimikizo chimene tinali
nacho pachiyambi. 15 Monga kunanenedwa kuti,
"Lero ngati mumva mawu ake,
musawumitse mitima yanu
ngati momwe munachitira pamene munawukira."

16 Nanga amene anamva ndi kuwukira anali ndani? Kodi si onse amene
Mose anawatulutsa mu Igupto? 17 Nanga amene Mulungu anawakwiyira
zaka makumi anayi anali ndani? Kodi si anthu amene anachimwa, amene
mitembo yawo inatsala m'chipululu muja? 18 Nanga Mulungu ankanena
za ndani kuti sadzalowa mu mpumulo wake? Pajatu ankanena za anthu
amene sanamvere aja. 19 Tsono ife tikuona kuti sanalowe chifukwa cha kusakhulupirika kwawo.

# 4

*Mpumulo wa Anthu a Mulungu*

1 Popeza lonjezo lakuti tidzalowe mu mpumulo umene anatilonjeza
lilipobe, tiyeni tisamale kuti pasakhale wina aliyense mwa inu wodza-
lephera kulowamo. 2 Pakuti Uthenga Wabwino unalalikidwa kwa ife,
monganso iwo aja; koma iwo sanapindule nawo uthengawo chifukwa
anangomva koma osakhulupirira. 3 Tsono ife amene takhulupirira talowa
mu mpumulo, monga momwe Mulungu akunenera kuti,
“Ndili wokwiya ndinalumbira kuti,
‘Iwo sadzalowa konse mu mpumulo wanga.’ ”
Ananena zimenezi ngakhale anali atatsiriza kale ntchito yolenga dziko
lapansi. 4 Pena pake wayankhula za tsiku lachisanu ndi chiwiri m’mawu
awa: “Pa tsiku lachisanu ndi chiwiri, Mulungu anapumula ku ntchito
zake zonse.” 5 Pa ndime inonso akunena za zomwezo pamene akuti, “Iwo
sadzalowa konse mu mpumulo wanga.”
6 Popeza kwatsalabe kuti ena adzalowe mu mpumulowo, koma aja
anayamba kumva Uthenga Wabwino sanalowe chifukwa cha kusamvera
kwawo. 7 N’chifukwa chake Mulungu anayikanso tsiku lina limene
analitcha “Lero.” Patapita nthawi yayitali Iye anayankhula za tsiku
lomweli kudzera mwa Davide, monga ndinanena kale kuti,
“Lero mukamva mawu ake,
musawumitse mitima yanu.”
8 Ngati Yoswa akanalowetsa anthu mu mpumulo, Mulungu sakananena
pambuyo pake za tsiku lina. 9 Kotero tsono kwatsala mpumulo wa Sabata
kwa anthu a Mulungu; 10 Pakuti aliyense amene analowa mu mpumulo wa
Mulungu anapuma pa ntchito zake, monga momwe Mulungu anachitira.
11 Tiyeni tsono tiyesetse kulowa mu mpumulo, kuti pasapezeke wina
aliyense wolephera potsatira chitsanzo chawo cha kusamvera.
12 Paja Mawu a Mulungu ndi amoyo ndi amphamvu. Ndi akuthwa
koposa lupanga lakuthwa konsekonse. Amalowa mpaka molumik-
izirana moyo ndi mzimu, ndiponso molumikizirana fundo ndi mafuta
a m’mafupa. Amaweruza malingaliro ndi zokhumba za m’mitima.
13 Palibe kanthu kobisika pamaso pa Mulungu. Zinthu zonse zili poyera
ndi zovundukuka pamaso pa Iye amene tiyenera kumufotokozera zonse
zimene tachita.

*Yesu Mkulu wa Ansembe Wopambana*

14 Popeza kuti tili ndi Mkulu wa ansembe wopambana, amene
analowa kale kumwamba, Yesu Mwana wa Mulungu, tiyeni tigwiritsitse
chikhulupiriro chathu chimene timavomereza. 15 Pakuti sitili ndi Mkulu
wa ansembe amene sangathe kutimvera chifundo chifukwa cha zofowoka
zathu. Koma tili naye amene anayesedwa m’njira zonse monga ife,
koma sanachimwe. 16 Tiyeni tsono tiyandikire ku mpando waufumu,
wachisomo mopanda mantha, kuti tilandire chifundo ndi kupeza chisomo
chotithandiza pa nthawi yeniyeni.

# 5

1 Mkulu wa ansembe aliyense amasankhidwa kuchokera pakati pa anthu
ndipo amayikidwa kuti aziwayimirira pamaso pa Mulungu, kuti azipereka
mphatso ndi nsembe chifukwa cha machimo. 2 Popeza kuti iye mwini ali
ndi zofowoka zake, amatha kuwalezera mtima amene ali osadziwa ndi

osochera. 3 Chifukwa cha ichi, iye amadziperekera nsembe chifukwa cha
machimo ake omwe ndiponso chifukwa cha machimo a anthu ena.
4 Palibe amene amadzipatsa yekha ulemu wotere, koma amachita
kuyitanidwa ndi Mulungu monga momwe anayitanidwira Aaroni.
5 N'chifukwa chake Khristu sanadzipatse yekha ulemu wokhala Mkulu wa
ansembe. Koma Mulungu anamuwuza kuti,
"Iwe ndiwe Mwana wanga;
Ine lero ndakhala Atate ako."
6 Ndipo penanso anati,
"Iwe ndiwe wansembe mpaka muyaya,
monga mwa unsembe wa Melikizedeki."
7 Yesu, pa nthawi imene anali munthu pa dziko lapansi pano, anapereka
mapemphero ake ndi zopempha mofuwula ndi misozi kwa Iye amene
akanamupulumutsa ku imfa, ndipo anamumvera chifukwa anagonjera
modzipereka. 8 Ngakhale Iye anali Mwana wa Mulungu anaphunzira
kumvera pomva zowawa. 9 Atasanduka wangwiro kotheratu, anakhala
gwero la chipulumutso chosatha kwa onse omvera Iye. 10 Ndipo Mulungu
anamuyika kukhala Mkulu wa ansembe, monga mwa dongosolo la
unsembe wa Melikizedeki.

### *Awachenjeza kuti Asataye Chikhulupiriro*

11 Tili ndi zambiri zoti tinganene pa zimenezi, koma ndi zovuta
kukufotokozerani chifukwa ndinu ochedwa kuphunzira. 12 Ngakhale kuti
pa nthawi ino munayenera kukhala aphunzitsi, pakufunikabe munthu
wina kuti abwerezenso kudzakuphunzitsani maphunziro oyambira a
choonadi cha Mulungu. Ndinu ofunika mkaka osati chakudya cholimba!
13 Aliyense amene amangodya mkaka okha, akanali mwana wakhanda,
sakudziwa bwino chiphunzitso cha chilungamo. 14 Koma chakudya
cholimba ndi cha anthu okhwima msinkhu, amene pogwiritsa ntchito
nzeru zawo, aphunzira kusiyanitsa chabwino ndi choyipa.

## 6

1 Tsono tiyeni tisangoyima pa maphunziro oyambirira enieni a Khristu
koma tipitirire kuti mukule msinkhu. Tisaphunzitsenso zinthu zomwe zili
ngati maziko, monga za kutembenuka mtima kusiya ntchito zosapindulitsa
pa moyo wosatha, za kukhulupirira Mulungu, 2 za maubatizo, za kusanjika
manja, za kuuka kwa akufa ndi za chiweruzo chotsiriza. 3 Ndipo Mulungu
akalola, tidzaterodi.
4 N'kosatheka kuwabwezanso anthu amene nthawi ina anawunikiridwa.
Iwowa analawapo mphatso yochokera kumwamba, n'kulandira nawo
Mzimu Woyera. 5 Analawa kukoma kwa mawu a Mulungu ndi mphamvu
za nthawi ikubwera. 6 Popeza anabwerera m'mbuyo, n'kosatheka kuti
atembenukenso mtima chifukwa akupachikanso Mwana wa Mulungu ndi
kumunyozetsa poyera.
7 Nthaka yolandira mvula kawirikawiri n'kubala mbewu zopindulitsa
oyilima, Mulungu amayidalitsa. 8 Koma nthaka yobereka minga ndi nthula
ndi yopanda phindu ndipo ili pafupi kutemberered wa. Matsiriziro ake
idzatenthedwa m'moto.
9 Okondedwa anga, ngakhale tikuyankhula zimenezi, ife tikudziwa kuti
muli nazo zinthu zabwino zomwe zimabwera pamodzi ndi chipulumutso.
10 Mulungu ndi wolungama, sangayiwale ntchito zanu ndi chikondi chanu

chimene munamuonetsa pothandiza anthu ake monga mmene muku-
chitirabe tsopano. [11] Ife tikufuna kuti aliyense wa inu aonetse changu
chomwechi mpaka kumapeto, kuti zichitikedi zomwe mukuyembekezera.
[12] Ife sitikufuna kuti inu mukhale aulesi, koma mutsatire anthu amene,
pokhulupirira ndi kupirira, akulandira zimene zinalonjezedwa.

### *Kukhazikika kwa Malonjezo a Mulungu*

[13] Pamene Mulungu ankamulonjeza Abrahamu, popeza panalibe
wamkulu womuposa, amene akanamutchula ndikulumbira mwa Iye,
analumbira mwa Iye yekha kuti, [14] "Ine ndidzakudalitsa ndithu, ndipo
ndidzakupatsa zidzukulu zambiri." [15] Ndipo Abrahamu atayembekezera
mofatsa, analandira zimene anamulonjezazo.

[16] Anthu amalumbira m'dzina la wina amene akuwaposa, ndipo lumbiro
lotere limatsimikizira zomwe zayankhulidwa ndi kuthetsa mikangano
yonse. [17] Momwemonso Mulungu pofuna kutsimikizira anthu amene
adzalandire lonjezo, kuti Iye sangasinthe maganizo, anatsimikiza lonjezo
lakelo ndi lumbiro. [18] Mulungu anachita zinthu ziwiri, lonjezo ndi
lumbiro, zimene sizingathe kusintha ndipo Mulungu sangathe kunama.
Choncho Mulungu akutilimbikitsa mtima ife amene tinathawira kwa Iye
kuti tichigwiritsitse chiyembekezo chimene tinalandira. [19] Chiyembekezo
chimenechi tili nacho ngati nangula wa moyo wathu. N'chokhazikika
ndi chosagwedezeka ndipo chimalowa m'katikati mwa malo opatulika,
kuseri kwa chinsalu chotchinga. [20] Yesu anatitsogolera kupita kumeneko,
nalowako m'malo mwathu. Iye anasanduka Mkulu wa ansembe onse
wamuyaya, monga mwa dongosolo la unsembe wa Melikizedeki.

# 7

### *Za Melikizedeki Mkulu wa Ansembe*

[1] Melikizedeki ameneyu anali mfumu ya ku Salemu, ndiponso
wansembe wa Mulungu Wammwambamwamba. Anakumana ndi Abra-
hamu pamene ankabwerera kuchokera ku nkhondo atagonjetsa mafumu
aja, Melikizedeki anakumana naye namudalitsa. [2] Ndipo Abrahamu
anamupatsa chakhumi cha zonse anafunkha. Choyamba dzina la Melik-
izedeki likutanthauza, "Mfumu ya chilungamo," kenakanso, "Mfumu ya
Salemu," kutanthauza, "Mfumu ya mtendere." [3] Alibe abambo kapena
mayi, alibe chiyambi kapena chitsiriziro cha moyo wake. Iye ali ngati
Mwana wa Mulungu ndipo akupitirira kukhala wansembe wamuyaya.

[4] Mukuona tsono kuti munthuyo anali wamkulu ndithu, pakuti Abra-
hamu kholo lathu anamupatsa chakhumi cha zimene anafunkha. [5] Tsono
lamulo likuti, ana a Levi amene amakhala ansembe azilandira chakhumi
kuchokera kwa Aisraeli, abale awo ngakhale kuti abale awowo ndi
ochokera kwa Abrahamu. [6] Melikizedeki sanali wochokera kwa Levi,
komabe analandira chakhumi kuchokera kwa Abrahamu nadalitsa Abra-
hamuyo amene analandira malonjezo a Mulungu. [7] Mosakayika konse,
munthu amene amadalitsa ndi wamkulu kuposa amene akudalitsidwayo.
[8] Ansembe amene amalandira chakhumi amafa, choncho Melikizedeki
ndi wamkulu kuwaposa iwo chifukwa Malemba amamuchitira umboni
kuti ndi wamoyo. [9] Wina angathe kunena kuti Levi, amene amalandira
chakhumi, anapereka chakhumicho kudzera mwa Abrahamu, [10] chifukwa
pamene Melikizedeki anakumana ndi Abrahamu n'kuti Levi ali m'thupi
la kholo lake.

### *Yesu Wofanana ndi Melikizedeki*

11 Kukanatheka kukhala wangwiro mwa unsembe wa Levi, pakuti
Malamulo anapatsidwa kwa anthu mwa unsembe wa Levi, n'chifukwa
chiyani panafunikanso wansembe wina kuti abwere, wofanana ndi
Melikizedeki, osati Aaroni? 12 Pakuti pamene unsembe usintha, mala-
mulonso amayenera kusintha. 13 Ambuye athu Yesu, amene mawuwa
akunena za Iye, anali wa fuko lina, ndipo palibe aliyense wochokera
fuko lakelo amene anatumikira pa guwa lansembe. 14 Pakuti n'zodziwika
bwino kuti Ambuye athu anachokera fuko la Yuda. Kunena za fuko
limeneli, Mose sananenepo kanthu za ansembe. 15 Ndipo zimene tanenazi
zimamveka bwino ngati tiona kuti pafika wansembe wina wofanana
ndi Melikizedeki. 16 Yesu sanakhale wansembe chifukwa cha malamulo
monga mwa mabadwidwe ake koma mwamphamvu ya moyo wosatha.
17 Pakuti Mulungu anamuchitira umboni kuti,

"Iwe ndi wansembe wamuyaya,
monga mwa dongosolo la unsembe wa Melikizedeki."

18 Choncho lamulo loyamba lachotsedwa chifukwa linali lofowoka ndi
lopanda phindu. 19 Tsono Malamulo sangathe kusandutsa chilichonse
kukhala changwiro, koma m'malo mwake mwalowa chiyembekezo chab-
wino, chimenechi timayandikira nacho kwa Mulungu.

20 Izi sizinachitiketu wopanda lumbiro. Ena ankakhala ansembe
popanda lumbiro. 21 Koma Yesu ankakhala wansembe ndi lumbiro
pamene Mulungu anati,

"Ambuye analumbira
ndipo sangasinthe maganizo ake,
'Iwe ndi wansembe wamuyaya.' "

22 Chifukwa cha lumbiroli, Yesu wakhala Nkhoswe ya Pangano lopambana.

23 Tsono ansembe akale aja analipo ambiri, popeza imfa imawale-
pheretsa kupitiriza ntchitoyi. 24 Koma Yesu popeza ndi wamuyaya,
unsembe wake ndi wosatha. 25 Chifukwa chake Iye amapulumutsa
kwathunthu amene amabwera kwa Mulungu kudzera mwa Iyeyo. Iye ali
ndi moyo nthawi zonse kuti adziwapempherera iwo.

26 Uyu ndi Mkulu wa ansembe amene tikumufuna chifukwa ndi
woyera, wopanda choyipa kapena chodetsa chilichonse, wosiyana ndi
anthu ochimwa, ndiponso wokwezedwa kuposa zonse zakumwambaku.
27 Kusiyana ndi akulu a ansembe ena aja, Yesu sanafunike kupereka
nsembe tsiku ndi tsiku poyamba chifukwa cha machimo ake, ndipo kenaka
chifukwa cha machimo a anthu ena. Iye anadzipereka nsembe chifukwa
cha machimo awo kamodzi kokha pamene anadzipereka yekha. 28 Pakuti
lamulo limasankha anthu amene ndi ofowoka kukhala akulu a ansembe;
koma lumbiro, lomwe linabwera pambuyo pa lamulo, linasankha Mwana,
amene anapangidwa kukhala wangwiro kwamuyaya.

## 8

### *Mkulu wa Ansembe wa Pangano Latsopano*

1 Fundo yayikulu pa zimene tikunenazi ndi iyi: Tili naye ife Mkulu
wa ansembe, amene anakhala ku dzanja lamanja la mpando waufumu
wa Mulungu Waulemerero kumwamba. 2 Ndipo akutumikira m'malo
opatulika, mu Tenti yeniyeni yoyikidwa ndi Ambuye, osati ndi munthu.

[3] Mkulu wa ansembe aliyense amasankhidwa kuti azipereka mphatso
ndi nsembe kwa Mulungu, ndipo kunali koyenera kuti wansembe
wathunso akhale n'kanthu kopereka. [4] Ngati iye akanakhala pa dziko la-
pansi, sakanakhala wansembe pakuti alipo kale anthu amene amapereka
mphatso zolembedwa m'Malamulo. [5] Iwo amatumikira pamalo opatulika
amene ndi chithunzi ndi chifanizo cha zimene zili kumwamba. Ichi ndi
chifukwa chake Mose anachenjezedwa pamene anali pafupi kumanga
Tenti: "Uwonetsetse kuti wapanga zonse monga momwe ndikukuonetsera
pa phiri pano." [6] Koma Yesu analandira utumiki wopambana kuposa
wawo monga Iyenso ali Nkhoswe ya pangano lopambana kuposa lakale
lija, chifukwa pangano latsopano lakhazikika pa malonjezano opambana
kwambiri.

[7] Ngati pangano loyamba lija likanakhala langwiro, sipakanafunikanso
lina m'malo mwake. [8] Koma Mulungu anapeza zolakwika pakati pa anthu
ndipo anati,

"Masiku akubwera," akutero Yehova,
"pamene ndidzachita pangano latsopano
ndi Aisraeli
ndiponso nyumba ya Yuda.
[9] Silidzakhala ngati pangano
limene ndinachita ndi makolo awo,
pamene ndinawagwira padzanja
n'kuwatulutsa ku Igupto
chifukwa iwo sanasunge pangano langa lija
ndipo Ine sindinawasamalire,
akutero Ambuye.
[10] Tsono ili ndi pangano ndidzapangane ndi nyumba ya Israeli:
Atapita masiku amenewa, akutero Ambuye,
Ine ndidzayika malamulo anga m'maganizo mwawo,
ndi kulemba m'mitima mwawo.
Ine ndidzakhala Mulungu wawo,
ndipo iwo adzakhala anthu anga.
[11] Sipadzafunikanso wina kuti aphunzitse mnzake,
kapena munthu kuphunzitsa m'bale wake, kunena kuti, udziwe Ambuye
chifukwa onse adzandidziwa,
kuyambira wamng'ono mpaka wamkulu.
[12] Pakuti Ine ndidzawakhululukira zoyipa zawo,
ndipo sindidzakumbukiranso machimo awo."

[13] Ponena kuti, pangano "latsopano" Mulungu wapanga pangano loy-
amba lija kukhala lotha ntchito, ndipo chilichonse chimene chayamba
kutha ntchito ndi kukalamba, chili pafupi kuchokeratu.

# 9

*Kupembedza m'Tenti ya Dziko Lapansi*

[1] Pangano loyamba lija linali ndi malamulo okhudza chipembedzo, ndi
malo opembedzeramo omangidwa ndi anthu. [2] Anthu ankamanga chi-
hema. M'chipinda choyamba munali choyikapo nyale, tebulo ndi buledi
woperekedwa kwa Mulungu. Chipinda chimenechi chinkatchedwa Malo
Opatulika. [3] Kuseri kwa chinsalu chotchinga chachiwiri kunkatchedwa
Malo Opatulika kwambiri. [4] M'menemo munali guwa lansembe lagolide

lofukizirapo lubani. Munalinso Bokosi la Chipangano lokutidwa ndi golide.
M'bokosimo munali m'phika wagolide m'mene ankasungiramo mana
ndi ndodo ya Aaroni imene inaphuka ija, ndiponso miyala ya pangano.
5 Pamwamba pa bokosilo panali zifanizo za angelo otchedwa akerubi
aulemerero, ataphimba chivundikiro cha bokosilo chimene chinali malo
okhulululukirapo machimo. Koma n'zosatheka tsopano kufotokoza zinthu
mwatsatanetsatane.

6 Zinthu zonsezi zitakonzedwa, ansembe ankalowamo m'chipinda choy-
amba chija nthawi ndi nthawi kumatumikiramo. 7 Koma Mkulu wa
ansembe yekha ndiye ankalowa chipinda chachiwiri chija kamodzi kokha
pa chaka. Iye sankalowamo wopanda magazi. Magaziwo ankapereka
nsembe kwa Mulungu chifukwa cha iye mwini ndiponso chifukwa cha
machimo a anthu amene ankachita mosazindikira. 8 Mwa njira imeneyi
Mzimu Woyera ankaonetsa kuti njira yolowera ku malo opatulika inali
isanaonetsedwe pamene Chihema choyamba chinali chilipo. 9 Zimenezi
n'zofanizira chabe, ndipo zinkalozera nthawi ino, kusonyeza kuti mphatso
ndi nsembe zimene zinkaperekedwa sizinkachotsa chikumbumtima cha
wopembedzayo. 10 Inali nkhani ya zakudya, ya zakumwa ndi ya miyambo
yosiyanasiyana ya masambidwe. Anali malamulo akunja kokha mpaka pa
nthawi imene anakonzanso zonse mwatsopano.

### *Magazi a Yesu*

11 Koma Khristu atafika monga Mkulu wa ansembe wa zinthu zokoma
zimene zilipo tsopano, Iye analowa m'Chihema chachikulu ndiponso
changwiro chimene sichinamangidwe ndi munthu, ndiye kuti sichili pansi
pano. 12 Iye sanalowemo ndi magazi ambuzi yayimuna, ana ang'ombe
amphongo, koma analowa Malo Opatulika kamodzi kokha ndi magazi
ake, atatikonzera chipulumutso chosatha. 13 Ngati magazi ambuzi yay-
imuna, ang'ombe yayimuna ndi phulusa la mwana wang'ombe wamkazi
zimati zikawazidwa pa odetsedwa zimawayeretsa kotero kuti amakhala
oyeretsedwa ku thupi, 14 n'koposa kotani magazi a Khristu, amene mwa
Mzimu wamuyaya anadzipereka yekha kwa Mulungu kukhala nsembe
yopanda chilema. Iye adzayeretsa chikumbumtima chathu pochotsa
ntchito za imfa, kuti ife titumikire Mulungu wamoyo.

15 Pa chifukwa chimenechi Khristu ndi m'khalapakati wa pangano
latsopano, kuti iwo amene anayitanidwa alandire chuma chamuyaya,
pakuti Iye tsopano anafa ngati dipo lomasula iwo ku machimo amene
anachita ali pansi pa pangano loyamba lija.

16 Ngati munthu alemba pangano losiyira ena chuma, pafunika kutsimik-
iza kuti wolemba panganolo wamwaliradi, 17 chifukwa pangano lotere
limakhala ndi mphamvu ngati wolembayo wamwalira. Siligwira ntchito
pamene wolembayo ali ndi moyo. 18 N'chifukwa chake pangano loyamba
lija silinachitike popanda kukhetsa magazi. 19 Mose atawawuza anthu
onse malamulo, anatenga magazi a ana ang'ombe amphongo ndi ambuzi
yayimuna pamodzi ndi madzi, ubweya wofiira ndiponso chitsamba
chotchedwa hisope, ndi kuwaza pa buku ndi anthu onse. 20 Iye anati, "Awa
ndi magazi a pangano limene Mulungu wakulamulirani kuti mulisunge."
21 Momwemonso Mose anawaza magazi pa Chihema chija ndiponso pa
zipangizo zonse zogwiritsa ntchito pa chipembedzo. 22 Monga mwa
malamulo titha kunena kuti, pafupifupi zinthu zonse zimayeretsedwa ndi
magazi ndipo popanda kukhetsa magazi palibe kukhululukidwa machimo.

23 Tsono panafunika kuti zinthu zingofanizira zenizeni za kumwamba,
ziyeretsedwe ndi nsembe zimenezi, koma zinthu za kumwamba zeniz-
enizo kuti ziyeretsedwe panafunika nsembe zina zoposa zimenezo.
24 Pakuti Khristu sanalowe m'malo opatulika omangidwa ndi anthu
amene anali chifaniziro cha malo enieniwo. Iye analowa kumwamba
kwenikweniko kuti azionekera pamaso pa Mulungu chifukwa cha ife.
25 Iye sanalowe kumwamba kuti azikadziperekanso nsembe kachiwiri
monga momwe mkulu wa ansembe ankachitira chaka ndi chaka ku Malo
Opatulika kwambiri ndi magazi amene sanali ake. 26 Zikanatero bwenzi
Khristu atamva zowawa kambirimbiri chilengedwere cha dziko lapansi.
Koma tsopano anaoneka kamodzi kokha chifukwa cha onse pa nthawi
yotsiriza kuti achotse tchimo podzipereka yekha nsembe. 27 Popeza
kunayikika kwa munthu kufa kamodzi ndipo kenaka kuweruzidwa,
28 momwemonso Khristu anadzipereka nsembe kamodzi kokha kuchotsa
machimo a anthu ambiri. Ndipo Iye adzaonekanso kachiwiri, osati kudza-
chotsa tchimo, koma kudzapereka chipulumutso kwa amene akumudikira.

# 10

*Yesu Nsembe ya Anthu Onse*

1 Malamulo ndi chithunzithunzi cha zinthu zabwino zimene zikubwera,
osati madalitso enieniwo. Pa chifukwa chimenechi sizingatheke konse kuti
nsembe zimodzimodzi, zoperekedwa kawirikawiri, kosalekeza ndi chaka
ndi chaka, kuti n'kusandutsa angwiro amene amabwera kudzapembedza.
2 Ngati zikanamatero iwowo akanasiya kupereka nsembezo. Pakuti opem-
bedzawo akanamayeretsedwa kamodzi kokha, sibwenzi chikumbumtima
chawo chikuwatsutsabe chifukwa cha machimo awo. 3 Koma nsembezo
zimawakumbutsa anthuwo machimo awo chaka ndi chaka. 4 Chifukwa
n'kosatheka kuti magazi ang'ombe yayimuna ndi mbuzi yayimuna achotse
machimo.

5 N'chifukwa chake Khristu atabwera pa dziko lapansi anati,

"Simunafune nsembe kapena zopereka,
koma thupi munandikonzera.
6 Simunakondwere nazo nsembe zopsereza
ndi nsembe zopereka chifukwa cha tchimo.
7 Tsono, Ine ndinati, 'Ndili pano Ine,
Inu Mulungu, ndabwera kudzachita zimene mukufuna monga zi-
nalembedwa m'Malemba.' "

8 Poyamba Iye anati, "Nsembe kapena zopereka zopsereza ndi nsembe
zopereka chifukwa cha tchimo, Inu simunazifune kapena kukondwera
nazo." Ngakhale kuti Malamulo ndiye amanena kuti ziperekedwe.
9 Pamenepo Iye anati, "Ndili pano Ine, ndabwera kudzachita zimene
mukufuna." Khristu anachotsa nsembe zoyamba zija kuti m'malo mwake
ayikemo nsembe za mtundu wachiwiri. 10 Chifukwa chakuti Yesu Khristu
anachita zimene Mulungu anafuna kuti achite, ndife oyeretsedwa ndi
nsembe ya thupi lake, limene analipereka kamodzi kokha.

11 Wansembe aliyense amayimirira tsiku ndi tsiku n'kutumikira, ndipo
amapereka nsembe imodzimodzi mobwerezabwereza, nsembe zimene
sizingathe kuchotsa machimo. 12 Koma pamene wansembe uyu anapereka
kamodzi kokha nsembe imodzi yokha chifukwa cha machimo, Iye
anakhala pansi ku dzanja lamanja la Mulungu. 13 Kumeneko akudikira

tsono kuti Mulungu asandutse adani ake kukhala chopondapo mapazi ake.
14 Chifukwa cha nsembe imodzi Iye anasandutsa angwiro kwamuyaya iwo
amene akuwayeretsa.
15 Mzimu Woyera nayenso akuchitira umboni za zimenezi kwa ife.
Poyamba Iye anati,
16 "Ili ndi pangano limene ndidzachita nawo
atapita masiku amenewo," akutero Yehova.
"Ndidzayika malamulo anga m'mitima mwawo,
ndipo ndidzawalemba m'maganizo mwawo."
17 Ndipo akutinso:
"Sindidzakumbukiranso konse
machimo awo ndi zolakwa zawo."
18 Ndipo pamene machimo akhululukidwa, sipafunikanso nsembe yop-
erekedwa chifukwa cha machimowo.

### *Kulimbika Mtima ndi Kupirira pa Chikhulupiriro*

19 Ndipo tsono abale, molimba mtima timalowa m'Malo Opatulika
kwambiri chifukwa cha magazi a Yesu. 20 Iye anatitsekulira njira
yatsopano ndi yamoyo kudutsa chinsalu chotchinga, chimene ndi thupi
lake. 21 Ndiponso tili ndi wansembe wamkulu woyang'anira nyumba ya
Mulungu. 22 Tsono tiyeni tiyandikire kwa Mulungu ndi mtima woona
ndi wodzaza ndi chikhulupiriro. Popeza mitima yathu yayeretsedwa,
ndi yopanda chikumbumtima chotitsutsa, ndiponso matupi athu asambit-
sidwa ndi madzi woyera. 23 Tiyeni tigwiritsitse mosagwedezeka zimene
timaziyembekezera ndi kuzivomereza, pakuti amene anatilonjezayo ndi
wokhulupirika. 24 Tiziganizira mmene tingalimbikitsirane wina ndi
mnzake pokondana ndi kuchita ntchito zabwino. 25 Tiyeni tisaleke
kusonkhana kwathu pamodzi monga mmene ena amachitira, koma
tizilimbikitsana makamaka poona kuti tsiku la Ambuye layandikira.
26 Ngati ife tipitirira kuchimwa mwadala pamene tikudziwa choona,
palibenso nsembe ina imene ingaperekedwe chifukwa cha machimo
athuwo. 27 Koma kumangodikira kokha ndi mantha chiweruzo ndiponso
moto woopsa umene udzawononga adani a Mulungu 28 Aliyense amene
amakana malamulo a Mose amaphedwa popanda n'chifundo chomwe,
malingana pali mboni ziwiri kapena zitatu. 29 Koposa kotani nanga ululu
wachilango chimene adzalandire munthu amene amapeputsa Mwana
wa Mulungu, amene amayesa magazi a pangano, amene anamuyeretsa,
kukhala chinthu chodetsedwa, ndi kunyoza Mzimu wachisomo? 30 Pakuti
timadziwa amene anati, "Kubwezera chilango n'kwanga; ndidzawalanga
ndine." Iye anatinso, "Ambuye adzaweruza anthu ake." 31 N'chinthu
choopsa kugwa m'manja a Mulungu wamoyo.
32 Kumbukirani masiku akale aja mutangowunikiridwa chatsopano, pa
nthawi imeneyi munapirira zowawa zambiri. 33 Nthawi zina ankakun-
yozani pagulu ndi kukuzunzani. Nthawi zina munkamva zowawa
pamodzi ndi amene ankasautsidwa chotere. 34 Munkawamvera chisoni
amene anali m'ndende ndiponso munkalola mokondwera kuti akulandeni
katundu wanu chifukwa munkadziwa kuti muli nacho chuma choposa ndi
chosatha.
35 Tsono musataye kulimbika mtima kwanuko pakuti mudzalandira
nako mphotho yayikulu. 36 N'kofunika kuti mupirire kuti pamene muchita
chifuniro cha Mulungu mudzalandire zimene Iye analonjeza. 37 Pakuti
n'kanthawi kochepa chabe,

Iye amene akubwera adzabwera ndipo sadzachedwa ayi.
38 Koma wolungama wangayo adzakhala ndi moyo mwachikhulupiriro.
Ndipo ngati iye abwerera m'mbuyo chifukwa cha mantha,
Ine sindidzakondwera naye.
39 Koma ife sindife amodzi a iwo obwerera m'mbuyo mwa mantha
ndi owonongedwa, koma ndife amodzi a amene akukhulupirira ndi
wopulumutsidwa.

# 11

*Za Chikhulupiriro cha anthu Akale*

1 Tsopano chikhulupiriro ndi kusakayika konse pa zinthu zimene
tikuziyembekeza, ndi kutsimikiza kuti zinthu zimene sitiziona
zilipo ndithu. 2 Ndi chikhulupiriro chimenechi makolo athu akale
anayamikidwa.
3 Ndi chikhulupiriro timazindikira kuti dziko lapansi ndi la mmwamba
zinapangidwa ndi Mawu a Mulungu, ndikuti zinthu zoonekazi zinachok-
era ku zinthu zosaoneka. 4 Ndi chikhulupiriro Abele anapereka kwa
Mulungu nsembe yoposa imene Kaini anapereka. Ndi chikhulupiriro
anatchedwa munthu wolungama Mulungu atayamikira zopereka zake.
Ngakhale iye anafa, akuyankhulabe chifukwa cha chikhulupiriro chake-
cho.
5 Ndi chikhulupiriro Enoki anatengedwa wamoyo, motero iye sanalawe
imfa; sanapezeke chifukwa Mulungu anamutenga. Pakuti asanatengedwe
anayamikiridwa kuti ankakondweretsa Mulungu. 6 Ndipo popanda
chikhulupiriro n'kosatheka kukondweretsa Mulungu, chifukwa aliyense
amene amabwera kwa Iye ayenera kukhulupirira kuti Mulungu alipodi
ndi kuti Iye amapereka mphotho kwa amene akumufunitsitsa.
7 Ndi chikhulupiriro, Nowa atachenjezedwa za zinthu zimene zinali
zisanaoneke, anachita mantha napanga chombo kuti apulumutsire banja
lake. Ndi chikhulupiriro chake anatsutsa dziko lapansi ndipo analandira
chilungamo chimene chimabwera ndi chikhulupiriro.
8 Ndi chikhulupiriro Abrahamu atayitanidwa kuti apite ku dziko limene
anamulonjeza kuti lidzakhala lake, anamvera ndi kupita, ngakhale
sanadziwe kumene ankapita. 9 Ndi chikhulupiriro chomwecho anakhala
ngati mlendo m'dziko lija limene Mulungu anamulonjeza. Anakhala
m'matenti monganso anachitira Isake ndi Yakobo, amene nawonso
analonjezedwanso. 10 Pakuti amadikira mudzi wokhala ndi maziko,
umene mmisiri ndi womanga wake ndi Mulungu.
11 Ndi chikhulupiriro Sara analandira mphamvu zokhala ndi pakati
ngakhale kuti zaka zake zobala mwana zinali zitapita kale, popeza
anamutenga amene analonjeza kukhala wokhulupirika. 12 N'chifukwa
chake mwa munthu mmodzi, amene anali ngati wakufa, munatuluka
mibado yochuluka ngati nyenyezi ndi yosawerengeka ngati mchenga wa
m'mbali mwa nyanja.
13 Onsewa anakhalabe mwachikhulupiriro mpaka anafa. Iwo sana-
landire zimene Mulungu anawalonjeza; iwo anangozionera chapatali ndi
kuzilandira. Ndipo iwo anavomereza kuti analidi alendo ndi osakhazikika
pa dziko lapansi. 14 Anthu amene amanena zinthu zotere amaonekeratu
kuti akufuna dziko lawo lenileni. 15 Akanakhala kuti akuganizira za
dziko limene analisiya akanapeza mpata obwerera kwawo. 16 M'malo
mwake, iwo amafunitsitsa dziko labwino, ndilo lakumwamba. N'chifukwa

chake Mulungu sachita manyazi kutchedwa Mulungu wawo, pakuti Iye
anawalonjeza mudzi.

17 Ndi chikhulupiriro Abrahamu, Mulungu atamuyesa, anapereka Isake
ngati nsembe. Ngakhale anali munthu woti Mulungu anamulonjeza,
anakhala wokonzeka kupereka nsembe mwana wake mmodzi yekhayo.
18 Za mwana ameneyu Mulungu anamuwuza iye kuti, "Zidzukulu zako
zidzachokera mwa Isake." 19 Abrahamu amazindikira kuti Mulungu
angathe kuukitsa akufa, ndipo tingathe kunena mofanizira kuti iye
analandiranso Isake ngati wouka kwa akufa.

20 Ndi chikhulupiriro Isake anadalitsa Yakobo ndi Esau pa zatsogolo
lawo.

21 Ndi chikhulupiriro, pamene Yakobo ankamwalira anadalitsa ana awiri
a Yosefe, ndipo anapembedza Mulungu atatsamira ndodo yake.

22 Ndi chikhulupiriro Yosefe ali pafupi kumwalira anayankhula za
kutuluka kwa Aisraeli mu Igupto ndipo anawawuza zoti adzachite ndi
mafupa ake.

23 Ndi chikhulupiriro Mose atabadwa makolo ake anamubisa miyezi
itatu, chifukwa iwo anaona kuti mwanayo anali wokongola ndipo sanaope
konse lamulo la mfumu.

24 Ndi chikhulupiriro Mose atakula, anakana kutchedwa mwana wa
mwana wamkazi wa Farao. 25 Iye anasankha kuzunzika nawo limodzi
anthu a Mulungu kuposa kusangalala ndi zokondweretsa za uchimo kwa
nthawi yochepa. 26 Anaona kuti kuzunzika chifukwa cha Khristu kunali
kwa mtengowapatali kuposa chuma cha ku Igupto, chifukwa amaona
mphotho ya m'tsogolo. 27 Ndi chikhulupiriro anachoka ku Igupto wosaopa
ukali wa mfumu. Iye anapirira chifukwa anamuona Mulungu amene ndi
wosaonekayo. 28 Ndi chikhulupiriro anachita Paska ndi kuwaza magazi,
kuti mngelo wowononga ana oyamba kubadwa asaphe ana oyamba
kubadwa a Aisraeli.

29 Ndi chikhulupiriro Aisraeli anawoloka Nyanja Yofiira ngati pa mtunda
powuma, koma Aigupto atayesa kutero anamizidwa.

30 Ndi chikhulupiriro mpanda wa Yeriko unagwa, Aisraeli atawuzun-
gulira kasanu ndi kawiri.

31 Ndi chikhulupiriro Rahabe, mkazi wadama sanaphedwe pamodzi ndi
osamvera aja chifukwa analandira bwino ozonda aja ku nyumba kwake.

32 Kodi ndinenenso chiyani? Nthawi yandichepera yoti ndinene za
Gideoni, Baraki, Samsoni, Yefita, Davide, Samueli ndi aneneri, 33 amene
ndi chikhulupiriro anagonjetsa mafumu, anakhazikitsa chilungamo ndi
kulandira zimene zinalonjezedwa. Anatseka pakamwa pa mikango,
34 anazimitsa moto waukali, ndipo anapulumuka osaphedwa ndi lupanga.
Anali ofowoka koma analandira mphamvu; anasanduka amphamvu pa
nkhondo, nathamangitsa magulu a ankhondo a adani awo. 35 Amayi ena
analandira anthu awo amene anafa, ataukitsidwanso. Enanso anazun-
zidwa ndipo anakana kumasulidwa, kuti adzaukenso ndi moyo wabwino.
36 Ena anawaseka ndi kuwakwapula, pamenenso ena anamangidwa ndi
kupita ku ndende. 37 Anagendedwa miyala; anachekedwa pakati; ena
anaphedwa ndi lupanga. Iwo anayendayenda atavala zikopa zankhosa
ndi zikopa zambuzi, umphawi okhaokha, ozunzidwa ndi kuvutitsidwa.
38 Dziko lapansi silinawayenere. Anayendayenda m'zipululu ndi mapiri,
ndiponso m'mapanga ndi m'maenje.

39 Onsewa anayamikidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo, komabe
palibe wa iwo amene analandira zimene analonjezedwa. 40 Mulungu
anatikonzera ife kanthu koposa, kuti iwo asayesedwe angwiro popanda
ife.

# 12

*Yesu Chitsanzo Chathu*

1 Tsono popeza ifenso tazunguliridwa ndi gulu lalikulu la mboni, tiyeni
titaye chilichonse chimene chimatitchinga, makamaka tchimo limene
limatikola mosavuta, ndipo tithamange ndi khama mpikisano umene
tayambawu. 2 Tiyeni tiyang'anitsitse Yesu, amene ndi woyamba ndi
wotsiriza wa chikhulupiriro chathu. Chifukwa cha chimwemwe chimene
chimamudikira anapirira zowawa zapamtanda. Iye ananyoza manyazi
a imfa yotere ndipo tsopano akukhala ku dzanja lamanja la mpando
waufumu wa Mulungu. 3 Muzilingalira za Iye amene anapirira udani
waukulu chotere wochokera kwa anthu ochimwa, kuti musafowoke ndi
kutaya mtima. 4 Polimbana ndi uchimo, simunafike mpaka pokhetsa
magazi.

*Mulungu Amalanga Ana ake*

5 Kodi mwayiwala mawu olimbitsa mtima aja, amene Mulungu
anayankhula kwa inu ngati ana ake? Mawuwo ndi awa:
"Mwana wanga, usapeputse kulanga kwa Ambuye
ndipo usataye mtima pamene akukudzudzula.
6 Chifukwa Ambuye amadzudzula amene amawakonda
ndipo amalanga aliyense amene amamulandira."
7 Pamene mukupirira masautso monga chilango, Mulungu achitira
inu monga ana ake. Kodi ndi mwana wotani amene abambo ake
samulanga? 8 Ngati inu simulangidwa, komatu aliyense amalangidwa,
ndiye kuti sindinu ana enieni koma am'chigololo. 9 Komanso, tonsefe tinali
ndi abambo athu otibala amene amatilanga ndipo timawapatsa ulemu.
Nanga kodi sitidzagonjera Atate a mizimu yathu kuti tikhale ndi moyo?
10 Abambo athu ankatilanga kwa kanthawi kochepa monga amaonera
kufunika kwake, koma Mulungu amatilanga kuti tipindule, kuti tikhale
oyera mtima. 11 Palibe chilango chimene chimaoneka kuti ndi chabwino
pa nthawiyo, komatu chowawa. Koma pambuyo pake, chimabweretsa
chipatso chachilungamo ndi mtendere kwa iwo amene aleredwa mwa
njira imeneyi.
12 N'chifukwa chake limbitsani manja anu otopa ndi mawondo anu
ogowoka. 13 Muziyenda m'njira zowongoka, kuti iwo amene akukutsati-
rani ngakhale ndi olumala ndi ofowoka asapunthwe ndi kugwa koma
adzilimbikitsidwa.

*Chenjezo kwa Okana Mulungu*

14 Yesetsani kukhala pa mtendere ndi anthu onse ndi kukhala oyera
mtima, pakuti popanda chiyero palibe ndi mmodzi yemwe adzaona
Ambuye. 15 Yang'anitsitsani kuti wina aliyense asachiphonye chisomo
cha Mulungu ndiponso kuti pasaphuke muzu wamkwiyo umene udzab-
weretsa mavuto ndi kudetsa ambiri. 16 Yang'anitsitsani kuti pasakhale
wina wachigololo. Kapena wosapembedza ngati Esau, amene chifukwa
cha chakudya cha kamodzi kokha anagulitsa ukulu wake. 17 Monga
inu mukudziwa, pambuyo pake pamene anafuna kuti adalitsidwe

anakanidwa. Sanapezenso mpata woti asinthe maganizo, ngakhale
anafuna madalitsowo ndi misozi.
18 Inu simunafike ku phiri limene mungathe kulikhudza, loyaka moto
wa mdima bii, la mphepo yamkuntho; 19 limene pali kulira kwa lipenga,
ndiponso kumveka kwa mawu. Anthu amene amamva mawuwo anapem-
pha kuti asawayankhulenso mawu ena. 20 Iwo anachita mantha ndi
lamulo lija lakuti, "Ngakhale nyama ikangokhudza phirilo, iphedwe ndi
miyala." 21 Maonekedwenso a Mose anali woopsa kwambiri, ngakhale
Mose yemwe anati, "Ine ndinachita mantha ndi kunjenjemera."
22 Koma inu mwafika ku Phiri la Ziyoni, ku mzinda wa Mulungu
wamoyo, Yerusalemu wakumwamba. Mwafika mu msonkhano wa angelo
osangalala osawerengeka. 23 Mwafika mu mpingo wa ana oyamba
kubadwa, amene mayina awo analembedwa kumwamba. Inu mwafika
kwa Mulungu, woweruza anthu onse, ndiponso kwa mizimu ya anthu
olungama ndi osandutsidwa kukhala angwiro. 24 Kwa Yesu m'khalapakati
wa pangano latsopano, ndiponso mwafika ku magazi owazidwa amene
amayankhula mawu abwino kuposa magazi a Abele.
25 Chenjerani kuti musakane kumvera amene akuyankhula nanu. Anthu
amene anakana kumvera iye amene anawachenjeza uja pa dziko lapansi
pano, sanapulumuke ku chilango ayi, nanga tsono ife tidzapulumuka
bwanji ngati tikufulatira wotichenjeza wochokera kumwamba? 26 Pa
nthawiyo mawu ake anagwedeza dziko lapansi, koma tsopano Iye
walonjeza kuti, "Kamodzi kenanso ndidzagwedeza osati dziko lapansi
lokha komanso thambo." 27 Mawu akuti, "Kamodzi kenanso," akuonetsa
kuchotsedwa kwa zimene zitha kugwedezeka, zonse zolengedwa, kotero
kuti zimene sizingatheke kugwedezeka zitsale.
28 Popeza tikulandira ufumu umene sungagwedezeke, tiyeni tikhale
oyamika ndi kupembedza Mulungu movomerezeka ndi mwaulemu ndi
mantha. 29 Pakuti Mulungu wathu ndi moto wonyeketsa.

# 13

### *Mawu Achilimbikitso Otsiriza*

1 Pitirizani kukondana monga abale. 2 Musayiwale kusamalira al-
endo, pakuti pochita zimenezi anthu ena anasamalira angelo amene
samawadziwa. 3 Muzikumbukira amene ali m'ndende ngati kuti inunso
ndi omangidwa, ndiponso amene akusautsidwa ngati inunso mukuvutika.
4 Ukwati muziwulemekeza nonse, ndipo mwamuna ndi mkazi azikhala
wokhulupirika, pakuti anthu adama ndi achigololo Mulungu adzawalanga.
5 Mtima wanu usakonde ndalama koma mukhutitsidwe ndi zimene muli
nazo, chifukwa Mulungu anati,
"Sadzakusiyani,
kapena kukutayani konse."
6 Kotero ife tikunena molimba mtima kuti,
"Ambuye ndiye mthandizi wanga;
sindidzachita mantha. Munthu angandichitenji ine?"
7 Muzikumbukira atsogoleri anu, amene amakulalikirani Mawu a
Mulungu. Ganizirani zamoyo wawo ndipo tsatirani chikhulupiriro chawo.
8 Yesu Khristu ndi yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zonse.
9 Musasochereseedwe ndi ziphunzitso zosiyanasiyana zachilendo.
N'kwabwino kuti mitima yathu ilimbikitsidwe ndi chisomo osati ndi
chakudya, chimene sichipindulitsa iwo amene amachidya. 10 Ife tili ndi

guwa lansembe, ndipo ansembe otumikira m'tenti cha Ayuda, saloledwa
kudya zochokera pamenepo.
11 Mkulu wa ansembe amatenga magazi kukapereka nsembe chi-
fukwa cha machimo, koma nyamayo imawotchedwa kunja kwa msasa.
12 N'chifukwa chakenso Yesu anafera kunja kwa mzinda kuti ayeretse
anthu ake kudzera m'magazi ake. 13 Tiyeni tsono, tipite kwa iye kunja kwa
msasa, titasenza chitonzo chake. 14 Pakuti ife tilibe mzinda wokhazikika
koma tikudikira mzinda umene ukubwera.
15 Tsono, tiyeni kudzera mwa Yesu tipereke nsembe zachiyamiko kwa
Mulungu osalekeza, chipatso cha milomo imene imavomereza dzina lake.
16 Ndipo musayiwale kumachita zabwino ndi kuthandiza ena, pakuti
Mulungu amakondwera ndi nsembe zotere. 17 Muzimvera atsogoleri anu
ndi kugonjera ulamuliro wawo, iwo amakuyang'anirani monga anthu
amene adzayenera kufotokoza za ntchito yawo pamaso pa Mulungu. Muzi-
wamvera kuti agwire ntchito yawo ndi chimwemwe osati molemedwa
pakuti izi sizingakupindulireni.
18 Mutipempherere ifenso. Pakuti tikutsimikiza kuti tili ndi chikumbum-
tima changwiro ndipo timafuna kuchita zinthu zonse mwaulemu. 19 Ine
ndikukupemphani kuti mundipempherere kuti Mulungu andibwezere
kwa inu msanga.
20 Mulungu wamtendere, amene kudzera m'magazi a pangano lamuyaya
anaukitsa Ambuye athu Yesu kwa akufa, amene ndi M'busa wamkulu,
21 akupatseni chilichonse chabwino kuti muchite chifuniro chake ndipo
Mulungu achite mwa ife, chimene chingamukomere kudzera mwa Yesu
Khristu. Kwa Iye kukhale ulemerero ku nthawi zanthawi, Ameni.
22 Ndikukupemphani abale kuti mulandire mawu anga achilimbikitso,
pakuti ndakulemberani mwachidule.
23 Ine ndikufuna kuti inu mudziwe kuti m'bale wathu Timoteyo
wamasulidwa. Ngati iye angafike msanga ndibwera naye kudzakuonani.
24 Mupereke moni kwa atsogoleri anu onse ndiponso kwa anthu onse a
Mulungu. Abale ochokera ku Italiya akupereka moni.
25 Chisomo chikhale ndi inu nonse.

# KALATA YA YAKOBO

1 Yakobo, mtumiki wa Mulungu ndi wa Ambuye Yesu Khristu,
kulembera mafuko khumi ndi awiri obalalikana ku mayiko
osiyanasiyana.
Landirani moni.

*Masautso ndi Mayesero*

2 Abale, muchiyese ngati chimwemwe chenicheni nthawi zonse pamene
mukukumana ndi mayesero amitundumitundu. 3 Inu mukudziwa kuti
kuyesedwa kwa chikhulupiriro chanu kumabweretsa chipiriro. 4 Chipiriro
chiyenera kugwira ntchito yake kuti mukhale okhwima ndi angwiro,
osasowa kanthu kalikonse. 5 Ngati wina pakati panu akusowa nzeru,
apemphe kwa Mulungu amene amapereka kwa onse mwaulere ndi
mosatonzera, ndipo adzapatsidwa. 6 Koma pamene mupempha, muyenera
kukhulupirira osakayika, chifukwa amene amakayika ali ngati mafunde
pa nyanja amene amawinduka nakankhika ndi mphepo. 7 Munthu wotere
asayembekezere kulandira kalikonse kuchokera kwa Ambuye. 8 Iyeyu ndi
munthu wa mitima iwiri, wosakhazikika pa zimene akuchita.
9 Abale omwe ndi anthu wamba anyadire pamene akwezedwa. 10 Koma
olemera anyadire pamene atsitsidwa, chifukwa adzatha ngati duwa
lakuthengo. 11 Pakuti dzuwa limatuluka n'kutentha kwake, ndipo
limafotetsa zomera. Duwa lake limathothoka ndipo kukongola kwake
kumatheratu. Momwemonso munthu wachuma adzazimirira ngakhale
atamachitabe malonda ake.
12 Wodala ndi munthu amene amapirira m'mayesero, chifukwa akapam-
bana adzalandira chipewa cha ulemerero chimene Mulungu analonjeza
anthu amene amamukonda.
13 Munthu akayesedwa asanene kuti, "Mulungu akundiyesa." Pakuti
Mulungu sangayesedwe ndi choyipa kapena Iyeyo kuyesa munthu
aliyense. 14 Koma munthu aliyense amayesedwa akakokedwa ndi zilako-
lako zake zoyipa ndi kukopedwa nazo. 15 Pamenepo, chilakolako chikakula
chimabala tchimo; ndipo tchimo likakhwima limabereka imfa.
16 Musanyengedwe abale anga okondedwa. 17 Mphatso iliyonse yabwino
ndi yangwiro imachokera kumwamba, kwa Atate mwini kuwala, amene
sasintha ngati mthunzi woyendayenda. 18 Iye anasankha kutibereka ife
kudzera m'mawu a choonadi, kuti pakati pa zolengedwa zake zonse,
tikakhale ngati zipatso zoyamba.

*Kumva ndi Kuchita*

19 Abale anga okondedwa, gwiritsitsani mawu awa: munthu aliyense
azifulumira kumva, koma asamafulumire kuyankhula, ndipo asamafu-
lumirenso kupsa mtima. 20 Pakuti mkwiyo wa munthu subweretsa
chilungamo chimene amafuna Mulungu. 21 Choncho chotsani chizolowezi
choyipa ndi khalidwe loyipa pakati panu, ndipo modzichepetsa landirani
mawu amene anadzalidwa mwa inu, amene akhoza kukupulumutsani.
22 Musamangomvetsera chabe mawu, ndi kumadzinyenga nokha. Chi-
tani zimene mawuwo amanena. 23 Munthu aliyense amene amangomva
mawu koma osachita zimene mawuwo amanena, ali ngati munthu amene

amayang'ana nkhope yake pa galasi. 24 Akadziyang'ana amachoka, nthawi
yomweyo n'kuyiwala mmene akuonekera. 25 Koma munthu amene
amayang'ana mwachidwi lamulo langwiro limene limapatsa ufulu ndi
kupitiriza kutero, osayiwala chimene wamva koma kuchita adzadalitsika
pa zimene amachita.

26 Ngati wina amadziyesa ngati ndi wachipembedzo, koma chonsecho
saletsa lilime lake, amadzinyenga yekha ndipo chipembedzo chake-
cho ndi cha chabechabe. 27 Chipembedzo chimene Mulungu Atate
athu amachivomereza kuti ndi changwiro ndi chopanda zolakwika ndi
ichi: kusamalira ana amasiye ndi akazi amasiye pa mavuto awo, ndi
kudzisunga bwino kuopa kudetsedwa ndi dziko lapansi.

# 2

*Kuchita Tsankho N'kosaloledwa*

1 Abale anga, okhulupirira Yesu Khristu waulemerero, musaonetse
tsankho. 2 Tangoganizirani, pakati panu patabwera munthu atavala
mphete yagolide ndi zovala zapamwamba, ndipo winanso wosauka
n'kulowa atavala sanza. 3 Ngati musamala kwambiri munthu wovala
bwinoyu uja, n'kumuwuza kuti, "Khalani pa mpando wabwinowu," koma
wosauka uja n'kumuwuza kuti, "Ima apo," kapena "Khala pansi pafupi ndi
chopondapo mapazi angawa," 4 kodi simunachite tsankho pakati panu ndi
kukhala oweruza a maganizo oyipa?

5 Tamverani abale anga okondedwa, kodi Mulungu sanasankhe
amene dziko lapansi limawaona ngati amphawi kuti akhale olemera
m'chikhulupiriro ndi kulowa ufumu umene Iye analonjeza kwa amene
amamukonda? 6 Koma mwakhala mukunyoza amphawi. Kodi si anthu
olemerawa amene akukudyerani masuku pamutu? Si anthu amenewa
amene amakukokerani ku bwalo la milandu? 7 Kodi si omwewa amene
amachita chipongwe dzina la wolemekezeka, limene inu mumatchulidwa?

8 Ngati musungadi lamulo laufumu lija lopezeka m'Malemba lakuti,
"Konda mnansi wako monga iwe mwini," ndiye kuti mukuchita bwino.
9 Koma mukamaonetsa tsankho mukuchimwa, ndipo ndinu wochimwa
monga wophwanya lamulo. 10 Pakuti amene amasunga Malamulo
onse, akangophwanya fundo imodzi yokha, waphwanya Malamulo onse.
11 Pakuti amene anati "Usachite chigololo" ndi yemweyonso anati
"Usaphe." Ngati suchita chigololo koma umapha, ndiwe wophwanya
Malamulo.

12 Muziyankhula ndi kuchita zinthu monga anthu amene mudza-
weruzidwe ndi lamulo limene limapereka ufulu, 13 chifukwa munthu
woweruza mopanda chifundo, nayenso adzaweruzidwa mopanda chi-
fundo. Chifundo chimapambana pa chiweruzo.

*Chikhulupiriro ndi Ntchito Zabwino*

14 Abale anga, phindu lake n'chiyani ngati munthu anena kuti ali ndi
chikhulupiriro koma chopanda ntchito zabwino? Kodi chikhulupiriro
choterechi chingamupulumutse? 15 Tangoganizirani, m'bale kapena
mlongo amene ali ndi usiwa, ndipo alibe chakudya cha tsiku ndi tsiku.
16 Ngati mmodzi wa inu amuwuza kuti, "Pita ndi mtendere, ukafundidwe
ndipo ukakhute," koma osamupatsa zimene akuzisowa, phindu lake
n'chiyani pamenepa? 17 Chomwechonso, chikhulupiriro chokha chopanda
ntchito zabwino ndi chakufa.

18 Koma wina anganene kuti, “Inuyo muli ndi chikhulupiriro koma ine
ndili ndi ntchito zabwino.”

Onetsani chikhulupiriro chanu chopanda ntchito zabwino ndipo in-
eyo ndidzakuonetsani chikhulupiriro changa pochita ntchito zabwino.
19 Mumakhulupirira kuti kuli Mulungu mmodzi yekha. Mumachita
bwino. Komatu ngakhale ziwanda zimakhulupirira zimenezi ndipo
zimanjenjemera ndi mantha.

20 Munthu wopusa iwe, kodi ukufuna umboni woti chikhulupiriro
chopanda ntchito zabwino n’chakufa? 21 Kodi Abrahamu kholo
lathu sanatengedwe kukhala wolungama chifukwa cha zimene anachita
pamene anapereka mwana wake Isake pa guwa lansembe? 22 Tsono
mukuona kuti chikhulupiriro chake ndi ntchito zabwino zinkachitika
pamodzi, ndipo chikhulupiriro chake chinasanduka chenicheni chifukwa
cha ntchito zake zabwino. 23 Ndipo Malemba akunena kuti, “Abrahamu
anakhulupirira Mulungu ndipo anatengedwa kukhala wolungama,” ndipo
anatchedwa bwenzi la Mulungu. 24 Tsono mukuona kuti munthu
amasanduka wolungama ndi ntchito zabwino osati ndi chikhulupiriro
chokha ayi.

25 N’chimodzimodzinso, kodi wadama uja, Rahabe, sanasanduke wol-
ungama chifukwa cha zomwe anachita pamene anapereka malo ogona
kwa azondi aja ndi kuwathawitsira mbali ina? 26 Monga thupi lopanda
mzimu ndi lakufa, chomwechonso chikhulupiriro chopanda ntchito zab-
wino ndi chakufa.

# 3

### *Za Lilime*

1 Abale anga, ambiri musakhale aphunzitsi chifukwa mumadziwa kuti
aphunzitsife tidzaweruzidwa mowuma kuposa anthu ena onse. 2 Tonsefe
timapunthwa m’njira zambiri. Ngati wina salakwa poyankhula, ameneyo
ndi munthu wangwiro, wodziwa kuyang’anira bwino thupi lake lonse.

3 Tikayika tizitsulo m’kamwa mwa akavalo kuti atimvere, timatha
kuwongolera thupi lake lonse. 4 Taonani sitima zapamadzi. Ngakhale ndi
zazikulu kwambiri ndipo zimakankhidwa ndi mphepo yamphamvu, zi-
mawongoleredwa ndi tsigiro laling’ono kulikonse kumene woyendetsayo
akufuna kupita. 5 Momwemonso, lilime ndi kachiwalo kakang’ono ka
thupi koma limadzitama kuti n’kuchita zikuluzikulu. Tangoganizirani za
nkhalango yayikulu imene ingapse ndi kalawi kamoto koyamba mochepa.
6 Lilime nalonso ndi moto, dziko la zoyipa pakati pa ziwalo za thupi.
Limawononga munthu yense wathunthu. Limayika zonse za moyo wake
pa moto, ndipo moto wake ndi wochokera ku gehena.

7 Mitundu yonse ya nyama, ya mbalame, ya zokwawa ndi ya zolengedwa
za m’nyanja, zikuwetedwa ndipo munthu wakhala akuziweta, 8 koma
palibe munthu amene angaweta lilime. Lilime ndipo silitha kupuma, ndi
lodzaza ndi ululu wakupha.

9 Ndi lilime lomwelo timatamanda Ambuye ndi Atate athu, komanso
ndi lilime lomwelo timalalatira anthu, amene anapangidwa m’chifanizo
cha Mulungu. 10 M’kamwa momwemo mutuluka matamando ndi kulalata.
Abale anga, zisamatero ayi. 11 Kodi madzi abwino ndi a mchere angatuluke
pa kasupe mmodzi? 12 Abale anga, kodi mtengo wa mkuyu n’kubala
mphesa, kapena mtengo wampesa n’kubala nkhuyu? Kasupe wa madzi
a mchere sangatulutsenso madzi abwino.

*Mitundu Iwiri ya Nzeru*

13 Ndani mwa inu amene ndi wanzeru ndi womvetsa zinthu? Mulekeni
aonetse ndi makhalidwe ake abwino kuti nzeru ndiye zikutsogolera
kudzichepetsa kwake ndi zochita zake 14 Koma ngati muli ndi mtima
wakaduka ndi odzikonda, musadzitamandire kapena kukana choonadi.
15 "Nzeru" zotere sizochokera kumwamba koma ndi za m'dziko lapansi,
si zauzimu koma ndi za ziwanda. 16 Pakuti pamene pali kaduka ndi
kudzikonda pomweponso pamakhala chisokonezo ndi zochitika zoyipa
zonse.

17 Koma nzeru imene imachoka kumwamba, poyamba ndi yangwiro,
ndi yokonda mtendere, yoganizira za ena, yogonjera, yodzaza ndi
chifundo ndi chipatso chabwino, yosakondera ndi yoona mtima. 18 Anthu
amtendere amene amadzala mtendere amakolola chilungamo.

# 4

*Kugonjera Mulungu*

1 N'chiyani chimene chimayambitsa ndewu ndi mapokoso pakati panu?
Kodi sizichokera ku zilakolako zimene zimalimbana m'kati mwanu?
2 Mumalakalaka zinthu koma simuzipeza, choncho mumapha. Mu-
masirira zinthu koma simutha kuzipeza zimene mukufuna, choncho
mumakangana ndi kumenyana. Mulibe zinthuzo chifukwa simupempha
kwa Mulungu. 3 Koma ngakhale mumapempha simulandira, chifukwa
mumapempha ndi zolinga zoyipa. Mumapempha kuti muzigwiritse
ntchito pa zokusangalatsani nokha.

4 Inu anthu achigololo, kodi simukudziwa kuti kuchita ubwenzi ndi
dziko lapansi ndi kudana ndi Mulungu? Choncho, aliyense wosankha
kukhala bwenzi la dziko lapansi amasanduka mdani wa Mulungu.
5 Kapena mukuganiza kuti Malemba amanena popanda chifukwa kuti
Mulungu amafunitsitsa mwansanje mzimu umene Iye anayika kuti
uzikhala mwa ife? 6 Koma amatipatsa chisomo chochuluka. N'chifukwa
chake Malemba amati,

"Mulungu amatsutsa odzikuza,
koma apereka chisomo kwa odzichepetsa."

7 Dziperekeni nokha kwa Mulungu. Mukaneni Mdierekezi ndipo
adzakuthawani. 8 Sendezani kufupi ndi Mulungu ndipo Iye adzasendeza
kwa inu. Sambani m'manja mwanu, inu anthu ochimwa. Yeretsani
mitima yanu, inu anthu okayikira. 9 Chitani chisoni chifukwa cha
zimene mwachita, lirani misozi. Kuseka kwanu kusanduke kulira, ndipo
chimwemwe chanu chisanduke chisoni. 10 Dzichepetseni pamaso pa
Ambuye ndipo Iye adzakukwezani.

11 Abale musamanenane. Aliyense wonenera zoyipa m'bale wake
kapena kumuweruza, akusinjirira ndi kuweruza Malamulo. Pamene
muweruza malamulo, ndiye kuti simukusunga malamulowo, koma
mukuwaweruza. 12 Pali mmodzi yekha Wopereka Malamulo ndi
Woweruza. Ndiye amene akhoza kupulumutsa ndi kuwononga. Kodi
ndiwe yani kuti uziweruza mnzako?

*Kunyadira za Mawa*

13 Tsono tamverani, inu amene mumati, "Lero kapena mawa tipita
ku mzinda wakutiwakuti, tikatha chaka chimodzi tikuchita malonda ndi
kupanga ndalama." 14 Chifukwa chiyani mukutero? Inu simukudziwa
zimene ziti zichitike mawa. Kodi moyo wanu ndi wotani? Inu muli

ngati nkhungu imene imangooneka kwa kanthawi kochepa ndipo kenaka
ndikuzimirira. 15 Koma inuyo muyenera kunena kuti, “Ambuye akalola,
tikadzakhala ndi moyo, tidzachita zakutizakuti.” 16 Koma mmene zililimu
mumangodzitama ndi kudzikuza. Kudzitama konse kotereku ndi koyipa.
17 Aliyense amene amadziwa zabwino zimene amayenera kuchita koma
osazichita, ndiye kuti wachimwa.

# 5

*Chenjezo kwa Achuma Opondereza Anzawo*

1 Tsono tamverani, inu anthu achuma, lirani ndi kufuwula chifukwa
cha zovuta zimene zidzakugwereni. 2 Chuma chanu chawola ndipo
njenjete zadya zovala zanu. 3 Golide ndi siliva wanu zachita dzim-
biri. Dzimbirilo lidzakhala umboni wokutsutsani ndi kuwononga mnofu
wanu ngati moto. Mwadziwunjikira chuma pa masiku ano otsiriza.
4 Taonani, ndalama za malipiro zimene munakanika kulipira aganyu aja
ankasenga m’munda mwanu zikulira mokutsutsani. Kulira kwa okololawo
kwamveka m’makutu mwa Ambuye Wamphamvuzonse. 5 Mwakhala
pa dziko lapansi pano moyo ofewa ndipo mwalidyera dziko lapansi.
Mwadzinenepetsa pa tsiku lokaphedwa. 6 Mwaweruza kuti ndi wolakwa
ndipo mwapha munthu wosalakwa, amene sakutsutsana nanu.

*Kupirira M’masautso*

7 Tsono abale, pirirani mpaka kubwera kwa Ambuye. Onani mmene
amachitira mlimi. Amadikirira kuti zipatso zabwino zioneke m’munda
mwake. Amayembekezera mokhazikika mtima kuyambira nthawi
ya mvula yoyamba mpaka yotsiriza. 8 Inunso mukhale owugwira
mtima ndi osasinthika chifukwa Ambuye ali pafupi kubwera. 9 Abale,
musamanenezane zoyipa kuopa kuti mungadzaweruzidwe. Woweruza ali
pa khomo!

10 Abale, tengerani chitsanzo cha aneneri amene anayankhula m’dzina
la Ambuye. Iwowo anakumana ndi zovuta koma anapirira. 11 Monga
mukudziwa, tinawatenga ngati odalitsika anthu amene anapirira. Mu-
namva za kupirira kwa Yobu ndipo mwaona zimene Ambuye anamuchi-
tira potsiriza pake. Ambuye ndi wodzaza ndi chisoni ndi chifundo.

12 Koposa zonse, abale anga, musamalumbire. Polumbira osamatchula
kumwamba kapena dziko lapansi, kapena china chilichonse. “Inde”
wanu azikhala “Inde,” ndipo “Ayi” wanu azikhala “Ayi,” kuopa kuti
mungadzapezeke olakwa.

*Pemphero la Chikhulupiriro*

13 Kodi alipo wina mwa inu amene ali pa mavuto? Apemphere. Kodi
wina wakondwa? Ayimbe nyimbo zolemekeza. 14 Kodi alipo wina mwa
inu akudwala? Ayitane akulu ampingo kuti adzamupempherere ndi ku-
mudzoza mafuta m’dzina la Ambuye. 15 Ndipo pemphero lachikhulupiriro
lidzachiritsa munthu wodwalayo ndipo Ambuye adzamuutsa. Ngati
wachimwa adzakhululukidwa. 16 Choncho, ululiranani machimo anu ndi
kupemphererana wina ndi mnzake kuti muchiritsidwe. Pemphero la
munthu wolungama ndi lamphamvu ndipo limagwira ntchito.

17 Eliya anali munthu ngati ife. Iye anapemphera mwamphamvu kuti
mvula isagwe ndipo sinagwedi kwa zaka zitatu ndi theka. 18 Kenaka
anapempheranso, ndipo kumwamba kunagwetsa mvula, ndipo dziko

lapansi linatulutsa zomera zake. 19 Abale anga, ngati mmodzi wa inu ap-
atuka pa choonadi ndipo wina wake ndi kumubweza, 20 kumbukirani izi:
Aliyense wobweza wochimwa kuchoka ku cholakwa chake, adzamupulu-
mutsa ku imfa ndi kukwirira machimo ambiri.

# KALATA YOYAMBA YA PETRO

1 Ndine Petro, mtumwi wa Yesu Khristu.
Ndikulemba kalatayi kwa onse osankhidwa ndi Mulungu, alendo
m'dziko lapansi, obalalikira ku Ponto, Galatiya, Kapadokiya, Asiya ndi
Bituniya. 2 Mulungu Atate anakusankhani, atakudziwani kuyambira
pachiyambi, ndipo Mzimu Woyera wakuyeretsani kuti mumvere Yesu
Khristu ndikutsukidwa ndi magazi ake.
Chisomo ndi mtendere zikhale ndi inu mochuluka.

## *Kuyamika Mulungu Chifukwa cha Chiyembekezo Chamoyo*

3 Alemekezedwe Mulungu, Atate wa Ambuye athu Yesu Khristu.
Mwachifundo chake chachikulu anatibadwitsa kwatsopano,
m'chiyembekezo chamoyo pomuukitsa Yesu Khristu kwa akufa,
4 kuti tidzalandire chuma chomwe sichingawonongeke, kuyipitsidwa
kapena kufota. Chuma chimenechi akukusungirani kumwamba.
5 Mwachikhulupiriro, mukusungidwa ndi mphamvu ya Mulungu mpaka
chipulumutso chitafika chimene chinakonzedwa kuti adzachionetse
nthawi yotsiriza. 6 Zimenezi zikukondweretseni kwambiri, ngakhale
tsopano, kwa kanthawi kochepa, mukumva zowawa m'mayesero
osiyanasiyana. 7 Mayeserowa abwera n'cholinga chakuti chikhulupiriro
chanu, chimene ndi chamtengo woposa wa golide, amene amawonongeka
ngakhale amayengedwa ndi moto, chitsimikizike kuti ndi chenicheni.
Pamenepo ndiye mudzalandire mayamiko, ulemerero ndi ulemu pamene
Yesu Khristu adzaoneka. 8 Ngakhale kuti simunamuone, mumamukonda;
ndipo ngakhale kuti simukumuona tsopano, mumamukhulupirira ndipo
mumakondwera ndi chimwemwe chachikulu ndi chosaneneka. 9 Motero
mukulandira mphotho ya chikhulupiriro chanu, ndiyo chipulumutso cha
moyo wanu.
10 Kunena za chipulumutso chimenechi, aneneri amene ananeneratu
za chisomo chimene chimabwera kwa inu, anafunafuna mofufuzafufuza
za chipulumutsochi, 11 kufuna kudziwa nthawi ndi momwe zidzachitikire
zinthu zimene Mzimu wa Khristu amene ali mwa iwo ankanenera za kuvu-
tika kwa Khristu, ndi ulemerero umene adzakhale nawo pambuyo pake.
12 Mulungu anawawululira kuti ntchito yawoyo sankayigwira chifukwa
cha iwo eni, koma chifukwa inu, pamene iwo ankayankhula zinthu zimene
mwamva tsopano kuchokera kwa amene amalalikira Uthenga Wabwino
mwamphamvu ya Mzimu Woyera wotumidwa kuchokera kumwamba.
Ngakhale angelo amalakalaka kuona nawo zinthuzi.

## *Khalani Oyera Mtima*

13 Choncho konzani mtima wanu, khalani odziretsa; khazikitsani
chiyembekezo chanu kotheratu pa chisomo chimene mudzapatsidwe
pamene Yesu Khristu adzaonekera. 14 Monga ana omvera, musatsatenso
zilakolako zoyipa zomwe munali nazo pamene munali osadziwa. 15 Koma
monga amene anakuyitanani ndi woyera, inunso khalani oyera mtima
m'makhalidwe anu wonse. 16 Pakuti, kwalembedwa kuti, "Khalani oyera
mtima, chifukwa Ine ndine Woyera."

[17] Popeza mumapemphera kwa Atate amene amaweruza munthu
aliyense mopanda tsankho molingana ndi zochita zake, pa nthawi imene
muli alendo pa dziko lapansi khalani moopa Mulungu. [18] Pakuti
mukudziwa kuti simunawomboledwe ndi zinthu zimene zimawonongeka
monga siliva kapena golide, kuchoka ku khalidwe lanu lachabe limene
munalandira kwa makolo anu. [19] Koma munawomboledwa ndi magazi
a mtengowapatali a Khristu, Mwana Wankhosa wopanda banga kapena
chilema. [20] Iye anasankhidwa lisanalengedwe dziko lapansi, koma
waonetsedwa chifukwa cha inu pa nthawi ino yotsiriza. [21] Kudzera mwa
Iye mumakhulupirira Mulungu, amene anamuukitsa kwa akufa namu-
patsa ulemerero. N'chifukwa chake chikhulupiriro ndi chiyembekezo
chanu chili mwa Mulungu.

[22] Tsopano mwayeretsa mitima yanu pomvera choonadi, kuti muzikon-
dana ndi abale anu, kukondana kwenikweni kochokera pansi pa mtima.
[23] Popeza mwabadwanso, osati ndi mbewu imene imawonongeka, koma
imene siwonongeka, ndiye kuti ndi Mawu a Mulungu amoyo ndi okhalitsa.
[24] Pakuti,

"Anthu onse ali ngati udzu,
ndipo ulemerero wawo uli ngati duwa la kuthengo.
Udzu umafota ndipo duwa limathothoka,
[25] koma mawu a Ambuye adzakhala mpaka muyaya."

Ndipo awa ndi mawu amene tinalalikira kwa inu.

# 2

[1] Choncho, lekani zoyipa zonse, chinyengo chilichonse, chiphamaso,
nsanje ndi kusinjirira kulikonse. [2] Monga makanda obadwa kumene
amalirira mkaka, inunso muzilakalaka mkaka weniweni wauzimu, kuti
mukule ndi kukufikitsani ku chipulumutso chanu, [3] pakuti tsopano
mwalawadi kuti Ambuye ndi wabwino.

### *Mwala wa Moyo ndi Anthu Osankhidwa*

[4] Pamene mukubwera kwa Iye, amene ndi Mwala wa moyo, umene
anthu anawukana, koma Mulungu anawusankha kuti ndi wa mtengowa-
patali, [5] inunso, mukhale ngati miyala ya moyo yoti Mulungu amangire
nyumba yake yauzimu kuti mukhale ansembe opatulika, opereka nsembe
zauzimu zovomerezeka ndi Mulungu mwa Yesu Khristu. [6] Pakuti
m'Malemba mwalembedwa kuti,

"Taonani, ndikuyika mwala wa maziko mu Ziyoni,
wosankhika ndi wamtengowapatali.
Amene akhulupirira Iye
sadzachititsidwa manyazi."

[7] Tsono kwa inu okhulupirira, mwalawo ndi wamtengowapatali. Koma
kwa amene sakhulupirira,

"Mwala umene amisiri anawukana
wasanduka mwala wa maziko,

[8] ndi

"Mwala wopunthwitsa anthu
ndiponso thanthwe limene limagwetsa anthu."

Iwo amapunthwa chifukwa samvera uthenga, pakuti ichi ndiye chinali
chifuniro cha Mulungu pa iwo.

[9] Koma inu ndinu anthu osankhidwa ndi Mulungu, ansembe achifumu,
mtundu woyera mtima, anthu ake enieni a Mulungu, munasankhidwa

kuti mulalikire za ntchito zamphamvu za Iye amene anakuyitanani
kuti mutuluke mu mdima ndi kulowa m'kuwunika kwake kodabwitsa.
10 Kale simunali anthu ake, koma tsopano ndinu anthu a Mulungu. Kale
simunalandire chifundo, koma tsopano mwalandira chifundo.

11 Okondedwa, ndikukupemphani, ngati alendo pansi pano, pewani
zilakolako za uchimo, zimene zimachita nkhondo ndi moyo wanu.
12 Khalani moyo wabwino pakati pa anthu osapembedza kuti ngakhale
atakusinjirirani kuti mumachita zoyipa, iwowo akaona ntchito zanu
zabwino, adzalemekeza Mulungu pa tsiku lomwe Iye adzatiyendere.

### *Kugonjera Olamulira*

13 Gonjerani maulamuliro onse chifukwa cha Ambuye. Kaya ndi
mfumu, imvereni chifukwa ili ndi ulamuliro waukulu, 14 kaya ndi
mabwanamkubwa, pakuti watumidwa ndi mfumu kuti alange onse amene
amachita zoyipa ndi kuyamikira onse amene amachita zabwino. 15 Pakuti
Mulungu akufuna kuti pochita ntchito zabwino muthetse kuyankhula
mosazindikira ndi mopusa. 16 Mukhale monga mfulu, koma musagwiritse
ntchito ufulu wanuwo ngati chophimbira zoyipa; mukhale monga atumiki
a Mulungu. 17 Chitirani ulemu aliyense, kondani abale okhulupirira,
wopani Mulungu, ndipo chitirani mfumu ulemu.

### *Akapolo*

18 Inu akapolo, gonjerani ambuye anu ndi kuwachitira ulemu, osati
kwa iwo okha amene ndi abwino ndi omvetsa zinthu, komanso kwa
amene ndi ankhanza. 19 Pakuti ndi chinthu chokoma ngati munthu apirira
mu zowawa zimene sizinamuyenera chifukwa chodziwa kuti Mulungu
alipo. 20 Kodi pali choti akuyamikireni ngati mupirira pomenyedwa
chifukwa choti mwalakwa? Koma ngati mumva zowawa chifukwa
chochita zabwino ndi kupirira, mwachita choyamikika pamaso pa Mu-
lungu. 21 Munayitanidwa kudzachita zimenezi, chifukwa Khristu anamva
zowawa chifukwa cha inu, anakusiyirani chitsanzo, kuti inu mutsatire
m'mapazi ake.

22 "Iye sanachite tchimo
    kapena kunena bodza."

23 Pamene anthu ankamuchita chipongwe, Iye sanabwezere chipongwe,
pamene Iye ankamva zowawa, sanaopseze. M'malo mwake, anadzipereka
kwa Mulungu amene amaweruza molungama. 24 Iye mwini anasenza
machimo athu m'thupi lake pa mtanda, kuti ife tife kutchimo ndi kukhala
ndi moyo potsata chilungamo, ndipo ndi mabala ake munachiritsidwa.
25 Pakuti munali monga nkhosa zosochera, koma tsopano mwabwerera
kwa m'busa ndi woyang'anira miyoyo yanu.

## 3

### *Akazi ndi Amuna*

1 Momwemonso, akazi inu gonjerani amuna anu kuti ngati ena a iwo
sakhulupirira Mawu a Mulungu, akopeke ndi makhalidwe a akazi awo
ndipo sipadzafunikanso mawu 2 pamene aona moyo wanu wachiyero
ndi moyo woopa Mulungu. 3 Kudzikongoletsa kwanu kusakhale kwa
maonekedwe akunja, monga kuluka tsitsi ndi kuvala zokometsera zagolide
ndi zovala zamberewere. 4 M'malo mwake kudzikongoletsa kwanu
kukhale kwa munthu wa m'katimo, kukongola kosatha kwa mtima ofatsa

ndi mzimu wachete, zimene ndi za mtengowapatali pamaso pa Mulungu.
5 Pakuti umo ndi mmene akazi oyera mtima akale amene anali ndi
chiyembekezo pa Mulungu anadzikongoletsera. Iwo ankagonjera amuna
awo, 6 monga Sara, amene anamvera Abrahamu namutcha iye mbuye
wake. Akazi inu ndinu ana ake ngati muchita zoyenera, ndipo musaope
choopsa chilichonse.

7 Momwemonso amuna inu, khalani mwanzeru ndi akazi anu, ndipo
muwachitire ulemu monga anzanu ofowoka ndiponso olandira nanu
pamodzi mphatso ya moyo wosatha, kuti pasakhale kanthu kotsekereza
mapemphero anu.

### *Kumva Zowawa Chifukwa cha Chilungamo*

8 Potsiriza, nonse khalani a mtima umodzi, omverana chisoni. Kon-
danani monga abale, muchitirane chifundo ndi kudzichepetsa. 9 Wina
akakuchitirani choyipa musabwezere pochitanso choyipa, kapena kub-
wezera chipongwe akakuchitirani chipongwe, koma muwadalitse. Mu-
nayitanidwa kuti mulandire mdalitso. 10 Pakuti,

"Iye amene angakonde moyo
ndi kuona masiku abwino,
aletse lilime lake kuyankhula zoyipa,
ndiponso milomo yake kunena mabodza.
11 Apewe zoyipa, ndipo azichita zabwino.
Afunefune mtendere ndi kuyesetsa kuwupeza.
12 Pakuti Ambuye amayang'anira bwino anthu olungama
ndipo amatchera khutu ku mapemphero awo.
Koma Ambuye sawayang'ana bwino amene amachita zoyipa."

13 Ndani angakuchitireni zoyipa ngati muchita changu kuchita zabwino?
14 Koma ngakhale mumve zowawa chifukwa cha chilungamo, ndinu
odala. "Musaope anthu, musachite mantha." 15 Koma lemekezani
Khristu m'mitima mwanu ngati Ambuye wanu. Khalani okonzeka
nthawi zonse kuyankha aliyense amene akufunsani za chiyembekezo
chimene muli nacho. 16 Koma chitani zimenezi mofatsa ndi mwaulemu,
mukhale ndi chikumbumtima chosakutsutsani, kuti anthu ena akanena
zoyipa za makhalidwe anu abwino mwa Khristu, achite okha manyazi
ndi chipongwe chawocho. 17 N'kwabwino ngati ndi chifuniro cha
Mulungu kumva zowawa chifukwa chochita zabwino kusiyana ndi kumva
zowawa chifukwa chochita zoyipa. 18 Pakuti Khristu anafa chifukwa cha
machimo kamodzi kokha kufera onse, wolungama kufera osalungama,
kuti akufikitseni kwa Mulungu. Anaphedwa ku thupi koma anapatsidwa
moyo mu mzimu. 19 Ndipo ali ngati mzimu chomwecho anapita ndi
kukalalikira mizimu imene inali m'ndende, 20 ya anthu amene sanamvere
Mulungu atadikira moleza mtima pa nthawi imene Nowa ankapanga
chombo. M'chombo chija anthu owerengeka okha, asanu ndi atatu,
ndiwo anapulumutsidwa ku madzi. 21 Madziwo akufanizira ubatizo
umene lero ukukupulumutsaninso, osati chifukwa chochotsa litsiro la
m'thupi koma chifukwa cha chikumbumtima choona pamaso pa Mulungu.
Umakupulumutsani chifukwa cha kuuka kwa Yesu Khristu, 22 amene
anapita kumwamba ndipo ali kudzanja lamanja la Mulungu komwe angelo
ndi maulamuliro ndi amphamvu amamvera Iye.

# 4

### *Moyo Watsopano*

1 Popeza kuti Khristu anamva zowawa m'thupi lake, mukhale nawonso
mtima omwewo, chifukwa iye amene wamva zowawa m'thupi lake
walekana nawo uchimo. 2 Chifukwa cha ichi, iwo sakhalanso moyo
wawo akuchita zofuna za matupi awo, koma amachita chifuniro cha
Mulungu. 3 Pakuti mwataya kale nthawi yambiri m'mbuyomu pochita
zimene anthu osapembedza amachita, moyo wokhumba zonyansa, zi-
lakolako zoyipa kuledzera, zochitika zoyipa za pa phwando, mapokoso
ndi kupembedza mafano onyansa. 4 Anthu osapembedza amadabwa
pamene simuthamangira nawo kuchita zoyipitsitsazi, n'chifukwa chake
amakuchitani chipongwe. 5 Koma adzafotokoza okha mlandu wawo kwa
Mulungu amene wakonzeka kuweruza amoyo ndi akufa. 6 Pa chifukwa
chimenechi, Uthenga Wabwino unalalikidwa ngakhale kwa iwo amene
tsopano ndi akufa, kuti adzaweruzidwe monga anthu ku thupi, koma
adzakhale ndi moyo monga mwa Mulungu mu mzimu.

7 Chimaliziro cha zinthu zonse chili pafupi. Choncho khalani maso
ndi odziletsa kuti muthe kupemphera. 8 Koposa zonse muzikondana
wina ndi mnzake kwambiri, chifukwa chikondi chimaphimba machimo
ambiri. 9 Muzisamalirana wina ndi mnzake osamanyinyirika. 10 Aliyense
agwiritse ntchito mokhulupirika mphatso iliyonse imene anayilandira
potumikira ena ngati adindo ogwiritsa bwino ntchito mphatso za Mulungu
za mitundumitundu. 11 Ngati wina ayankhula, ayankhuledi mawu enieni a
Mulungu. Ngati wina atumikira, atumikire ndi mphamvu imene Mulungu
amapereka, kuti pa zonse Mulungu alemekezedwe mwa Yesu Khristu. Kwa
Iye kukhale ulemerero ndi mphamvu mpaka muyaya, Ameni.

### *Kumva Zowawa Chifukwa cha Chikhristu*

12 Abale okondedwa musadabwe ndi mayesero owawa amene mukuku-
mana nawo ngati kuti china chake chachilendo chakuchitikirani. 13 Koma
kondwerani popeza mukumva zowawa pamodzi ndi Khristu, kuti mudza-
kondwere kwakukulu pamene ulemerero wake udzaonekera. 14 Ngati
akuchitani chipongwe chifukwa cha dzina la Khristu, ndinu odala, ndiye
kuti Mzimu waulemerero wa Mulungu uli pa inu. 15 Ngati mumva
zowawa, zisakhale chifukwa cha kupha munthu, kapena kuba, kapena
kuchita choyipa, kapena kulowerera za anthu ena, 16 koma ngati mumva
zowawa chifukwa ndinu Mkhristu, musachite manyazi, koma muyamike
Mulungu chifukwa cha dzinalo. 17 Pakuti nthawi yafika kuti chiweruzo
chiyambe m'nyumba ya Mulungu, ndipo ngati chiyamba ndi ife nanga
podzafika kwa osamvera Uthenga Wabwino wa Mulungu, chidzakhala
chotani? 18 Monga Malemba akuti,
"Ngati kuli kovuta kuti olungama apulumuke,
nanga munthu wochimwa, wosasamala za Mulungu adzatani?"

19 N'chifukwa chake, iwo amene akumva zowawa monga mwa chi-
funiro cha Mulungu, adzipereke okha m'manja mwa Mlengi wawo
wokhulupirika ndi kumapitiriza kuchita zabwino.

# 5

### *Akulu Ampingo ndi Anyamata mu Mpingo*

1 Ine ndikupempha akulu a mpingo amene ali pakati panu, monga
inenso mkulu mnzawo, mboni ya zowawa za Khristu ndiponso amene
ndidzalandira nawo ulemerero umene uti udzaonetsedwe. 2 Wetani gulu
la Mulungu limene lili m'manja mwanu, muziliyang'anira. Muzichita osati
mowumirizidwa, koma mwakufuna kwanu, monga momwe Mulungu
akufunira kuti mutero. Musachite chifukwa chadyera la ndalama, koma
ndi mtima ofuna kutumikira. 3 Musakhale ngati mafumu pa amene
mukuwayang'anira, koma mukhale chitsanzo kwa gululo. 4 Ndipo
M'busa wamkulu akadzaonekera, mudzalandira chipewa cha ulemerero
chosafota.

5 Momwemonso, inu anyamata gonjerani amene ndi akulu. Inu nonse
mukhale odzichepetsa kuti mutumikirane, chifukwa,

"Mulungu amatsutsana nawo odzikuza,
koma amapereka chisomo kwa odzichepetsa."

6 Choncho, mudzichepetse pamaso pa Mulungu wamphamvu, kuti pa
nthawi yake adzakukwezeni. 7 Tayani pa Iye nkhawa zanu zonse chifukwa
ndiye amakusamalani.

8 Khalani odziretsa ndi atcheru. Mdani wanu mdierekezi
amayendayenda monga mkango wobangula kufunafuna wina kuti
amumeze. 9 Mukaneni iye, ndipo mukhazikike m'chikhulupiriro,
chifukwa mukudziwa kuti abale anzanu pa dziko lonse lapansi nawonso
akumva zowawa zomwezi.

10 Ndipo Mulungu wachisomo chonse, amene anakuyitanani ku ulemerero wake wamuyaya mwa Khristu, mutamva zowawa pa kanthawi,
adzakukonzaninso ndi kukulimbitsani pa maziko olimba. 11 Kwa Iye
kukhale mphamvu mpaka muyaya, Ameni.

## *Mawu Otsiriza*

12 Mothandizidwa ndi Sila, amene ndi m'bale wokhulupirika, ndakulemberani mwachidule kukulimbikitsani ndi kuchita umboni kuti ichi ndi
chisomo choona cha Mulungu. 13 Imani mwamphamvu m'chisomochi.
Mlongo wanu amene ali ku Babuloni, wosankhidwa pamodzi nanu
akupereka moni, nayenso Marko, mwana wanga, akupereka moni.
14 Mupatsane moni ndi mpsopsono wachikondi. Mtendere ukhale ndi inu
nonse amene muli mwa Khristu.

# KALATA YACHIWIRI YA PETRO

1 Ndine Simoni Petro, mtumiki ndi mtumwi wa Yesu Khristu.
Kwa anthu amene analandira chikhulupiriro cha mtengowapatali
chomwe ifenso tinalandira chifukwa cha chilungamo cha Mulungu ndi
Mpulumutsi wathu Yesu Khristu.

2 Chisomo ndi mtendere zochuluka zikhale nanu pomudziwa Mulungu
ndi Yesu Ambuye athu.

### *Kudziwa za Mayitanidwe ndi za Kusankhidwa Kwathu*

3 Mulungu mwa mphamvu zake anatipatsa zonse zofunika kukhala
moyo opembedza, potidziwitsa za Iyeyo amene anatiyitana ku ulemerero
wake ndi ubwino wake. 4 Mwa ulemerero ndi ubwino wakewo, anatipatsa
malonjezo opambana kwambiri ndi a mtengowapatali. Amenewa ndi
malonjezo amene amakuthandizani kulandira nawo moyo wa Mulungu,
titapulumuka ku chiwonongeko chimene chili m'dziko lapansi chifukwa
cha zilakolako zoyipa.

5 Choncho, chitani khama kuwonjezera moyo wabwino pa
chikhulupiriro chanu, ndipo pa moyo wabwino muwonjezerepo nzeru.
6 Pa nzeru muwonjezerepo kudziretsa, pa kudziretsa muwonjezerepo
chipiriro, ndipo pa chipiriro muwonjezerepo khalidwe lolemekeza
Mulungu. 7 Pa khalidwe lolemekeza Mulungu muwonjezerepo chifundo
cha ubale, pa chifundo cha ubale muwonjezerepo chikondi. 8 Ngati zonsezi
zikhala mwa inu n'kumachuluka, zidzakuthandizani kuti musakhale
aulesi ndi osapindula ndi chidziwitso chanu cha Ambuye athu Yesu
Khristu. 9 Koma ngati wina alibe zimenezi, ndi wakhungu sangathe
kuona patali, ndipo wayiwala kuti anayeretsedwa machimo ake akale.

10 N'chifukwa chake abale anga, funitsitsani kuti mayitanidwe ndi
masankhidwe anu akhale otsimikizika. Pakuti ngati muchita zinthu izi,
simudzagwa konse. 11 Mudzalandiridwa bwino kwambiri mu ufumu
wosatha wa Ambuye ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu.

### *Kukhala Oyera Mtima*

12 Tsono ine ndidzakukumbutsani nthawi zonse za zinthu zimenezi,
ngakhale kuti mumazidziwa ndipo kuti munakhazikika m'choonadi
chimene muli nacho tsopano. 13 Ndikuganiza kuti n'koyenera ndikanali
mu msasa uno, kuti ndikutsitsimutseni ndi kukukumbutsani, 14 chifukwa
ndikudziwa kuti posachedwapa ndikuchoka mu msasa uno, monga
Ambuye athu Yesu Khristu anandidziwitsiratu. 15 Ndipo ndidzayesetsa
kuti nditachoka, mudzakumbukire nthawi zonse.

16 Ife sitinatsate nkhani zongopeka titakuwuzani za mphamvu zake
ndi zakubweranso kwa Ambuye athu Yesu Khristu, koma tinaona ndi
maso athu za ukulu wake. 17 Pakuti Iye analandira ulemu ndi ulemerero
kuchokera kwa Mulungu Atate atamufikira mawu ochokera ku ulemerero
wa ukulu akuti, "Uyu ndi mwana wanga amene Ine ndimukonda, amene
ndimakondwera naye kwambiri." 18 Ifeyo tinamva mawuwa akuchokera
kumwamba pamene tinali naye pamodzi pa phiri lopatulika lija.

19 Tsono ifenso tili ndi mawu a uneneri amene ndi odalirika kwambiri
ndipo inu mudzachita bwino mukawasamalira mawuwa, monga kuwu-
nika kumene kukuwala mu mdima, mpaka tsiku lidzayambe kucha,
pamene nthanda idzayambe kuwala m'mitima mwanu. 20 Kuposa
zonse, inu muyenera kuzindikira kuti palibe mawu a uneneri amene
amatanthauzidwa pa okha. 21 Pakuti mawu a uneneri sanadze mwa
kufuna kwa anthu, koma anthu anayankhula zochokera kwa Mulungu,
Mzimu Woyera atawayankhulitsa.

# 2

*Aphunzitsi Onyenga*

1 Koma panalinso aneneri onama pakati pa Aisraeli, monga
padzakhalanso aphunzitsi onyenga pakati panu. Iwo adzalowetsa
mwamseri ziphunzitso zonama ndi zowononga, nadzakana Ambuye
amene anawawombola, ndipo motero adzadziyitanira okha
chiwonongeko mwadzidzidzi. 2 Ambiri adzatsata njira zawo zochititsa
manyazi ndipo chifukwa cha iwowa, anthu adzanyoza njira ya choonadi.
3 Pofuna kupeza chuma, aphunzitsiwa adzakudyerani chuma chanu
pokuwuzani nkhani zopeka. Chiweruzo chawo chinakonzedwa kale,
ndipo chikuwadikira.

4 Pakuti Mulungu sanalekerere angelo atachimwa paja, koma
anawaponya m'ndende, nawayika m'maenje amdima, kuwasunga
kuti adzaweruzidwe. 5 Iye sanalekerere dziko lapansi kalelo, koma
anapulumutsa Nowa, mlaliki wa chilungamo, ndi anthu ena asanu
ndi awiri atadzetsa chigumula pa dziko lapansi kwa anthu akhalidwe
losapembedza Mulunguyo. 6 Mulungu anaweruza mizinda ya Sodomu
ndi Gomora nayiwononga ndi moto, kuti ikhale chitsanzo cha zimene
zidzachitikira anthu osapembedza Mulungu. 7 Koma Iye anapulumutsa
Loti, munthu wolungama, amene ankavutika ndi khalidwe lonyansa la
anthu oyipa. 8 (Pakuti munthu wolungamayo, pokhala pakati pawo
tsiku ndi tsiku ankavutika mu mtima ndi makhalidwe awo oyipa
amene ankawaona ndi kuwamva). 9 Tsono mutha kuona kuti Ambuye
amadziwa kuwapulumutsa kwake pa mayesero anthu opembedza.
Amadziwanso kusunga osalungama kuti alangidwe mpaka tsiku la
chiweruzo. 10 Makamaka amene amatsata zilakolako zonyansa zathupi
nanyoza ulamuliro.

Anthu amenewa ndi odzikuza, ndipo otsata chifuniro cha iwo
eni, sasamala za munthu, saopa kuchitira chipongwe zolengedwa za
mmwamba. 11 Komatu ngakhale angelo, amene ali akulu ndi amphamvu
kuwaposa, sayankhula za chipongwe pobweretsa chiweruzo pa iwo
kuchokera kwa Ambuye. 12 Koma anthu awa amachita chipongwe
zinthu zimene sakuzidziwa. Ali ngati zirombo zopanda nzeru. Zirombo
zolengedwa kuti zigwidwe ndi kuwonongedwa, ndipo ngati zirombozo
adzawonongedwa.

13 Iwo adzalangidwa chifukwa cha zoyipa zimene anachita. Koma
chimene chimawakomera ndi kumangochita zokondweretsa thupi
masanasana. Iwo ali ngati mawanga ndi zilema. Podya nanu pamodzi
amakondwera kuchita za chinyengo. 14 Ndi maso awo odzaza ndi
chigololo, salekeza kuchimwa. Amanyengerera anthu osakhazikika. Iwo
ndi akatswiri pa dyera ndi chuma, ndipo ndi ana otembereredwa! 15 Iwo
anasiya njira yolungama ndipo anapatuka kutsata njira ya Baalamu

mwana wa Beori, amene anakonda malipiro a chosalungama. [16] Koma
anadzudzulidwa chifukwa cha kulakwa kwakeko. Bulu, nyama imene
siyankhula, inayankhula ngati munthu kuletsa misala ya mneneriyo.

[17] Anthu amenewa ali ngati akasupe wopanda madzi, ndiponso ngati
nkhungu yowuluzidwa ndi mphepo yamkuntho. Mulungu wawasungira
mdima wandiweyani. [18] Pakuti anayankhula mawu opanda pake ndi
onyada, ndipo ndi zilakolako zoyipa za thupi amanyenga anthu amene
angopulumuka kumene pakati pa anzawo oyipa. [19] Amawalonjeza
ufulu, pomwe iwo eni ndi akapolo a zizolowezi zowononga. Pajatu
munthu amakhala kapolo wa chilichonse chimene chikumulamulira.
[20] Ngati anapulumuka ku zodetsa za dziko lapansi podziwa Ambuye
ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu, pambuyo pake nagwidwanso ndi
kugonjetsedwa ndi zomwezo, potsiriza adzakhala oyipa kuposa mmene
analili poyamba. [21] Kukanakhala bwino akanapanda kudziwa njira ya
chilungamo, koposa ndi kuyileka atadziwa lamulo loyera limene Mulungu
anawapatsa. [22] Kwa iwo miyambi iyi ndi yoona, "Galu wabwerera ku
masanzi ake," ndipo, "Nkhumba imene inasamba, yakunkhunizikanso
m'matope."

# 3

*Kubwera kwa Ambuye*

[1] Inu okondedwa, iyi ndi kalata yanga yachiwiri kwa inu. Ine ndalemba
makalata onse awiri kuti ndikukumbutseni ndi kukutsitsimutsani ndi
cholinga choti muzilingalira moyenera. [2] Ndikufuna kuti mukumbukire
mawu amene anayankhulidwa kale ndi aneneri oyera mtima ndiponso
lamulo limene Ambuye ndi Mpulumutsi wathu analipereka kudzera mwa
atumwi.

[3] Poyamba mudziwe kuti m'masiku otsiriza kudzafika anthu onyoza,
adzanyoza ndi kutsata zilakolako zawo zoyipa. [4] Iwo adzati, "Kodi suja
Ambuye analonjeza kuti adzabweranso? Nanga ali kuti? Lija n'kale
anamwalira makolo athu, koma zinthu zonse zili monga anazilengera
poyamba paja." [5] Koma iwo akuyiwala dala kuti Mulungu atanena
mawu, kumwamba kunakhalapo ndipo analenga dziko lapansi ndi madzi.
[6] Ndi madzinso achigumula, dziko lapansi la masiku amenewo lina-
wonongedwa. [7] Dziko la kumwamba ndi lapansi la masiku ano akulisunga
ndi mawu omwewo kuti adzalitentha ndi moto. Akuzisunga mpaka tsiku
limene adzaweruza ndi kuwononga anthu onse osapembedza Mulungu.

[8] Koma abale okondedwa, musayiwale chinthu chimodzi ichi: Kuti
pamaso pa Ambuye tsiku limodzi lili ngati zaka 1,000, ndipo zaka
1,000 zili ngati tsiku limodzi! [9] Ambuye sazengereza kuchita zimene
analonjeza, monga ena amaganizira. Iwo akukulezerani mtima, sakufuna
kuti aliyense awonongeke, koma akufuna kuti aliyense alape.

[10] Koma tsiku la Ambuye lidzafika ngati mbala. Pa tsikuli zinthu
zakumwamba zidzachoka ndi phokoso lalikulu. Zinthu zonse zidza-
wonongedwa ndi moto, ndipo dziko lapansi ndi zonse zili m'menemo
zidzapsa.

[11] Popeza kuti zinthu zonse zidzawonongedwa motere, kodi inu muyen-
era kukhala anthu otani? Muyenera kukhala moyo wachiyero ndi
opembedza Mulungu [12] pamene mukuyembekezera tsiku la Mulungu ndi
kufulumiza kufika kwake. Pa tsiku limeneli zinthu zakumwamba zidza-
wonongedwa ndi moto, ndipo zidzasungunuka ndi kutentha. [13] Koma ife

tikudikira kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano, zimene
Mulungu analonjeza, m'mene chilungamo chidzakhalamo.
14 Chomwecho okondedwa, popeza inu mukudikira zimenezi, chitani
changu kuti mukhale wopanda chilema kuti mukhale pa mtendere ndi
Iye. 15 Zindikirani kuti kuleza mtima kwa Ambuye kukutanthauza chip-
ulumutso, monga momwe m'bale wathu wokondedwa Paulo anakulem-
beraninso ndi nzeru zimene Mulungu anamupatsa. 16 Iye walemba
chimodzimodzi makalata ake onse, kuyankhula za zinthu izi. M'makalata
ake mumakhala zinthu zina zovuta kuzimvetsa, zimene anthu osadziwa
ndi osakhazikika amazipotoza, monga amachita ndi malemba ena onse,
potero akudziwononga okha.
17 N'chifukwa chake, abale okondedwa, popeza mukuzidziwa kale
zimenezi, chenjerani kuti musatengeke ndi zolakwa za anthu osaweruzika,
mungagwe ndi kuchoka pamalo otetezedwa. 18 Koma kulani mu chisomo
ndi m'chidziwitso cha Ambuye ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khristu. Kwa
Iye kukhale ulemerero tsopano mpaka muyaya. Ameni.

# KALATA YOYAMBA YA YOHANE

*Mawu a Moyo*

1 Tikukulalikirani za Mawu a moyo amene analipo kuyambira
pachiyambi, amene tinawamva, amene tinawaona ndi maso athu, amene
tinawapenyetsetsa, ndipo tinawakhudza ndi manja athu. 2 Moyowo
unaoneka, tinawuona ndipo tikuchitira umboni. Tikukulalikirani za
moyo wosatha umene unali ndi Atate ndipo unaonekera kwa ife.
3 Tikukulalikirani chimene tinachiona ndi kumva, kuti inuyo muyanjane
nafe. Kuyanjana kwathu, tikuyanjana ndi Atate ndiponso ndi Mwana
wawo, Yesu Khristu. 4 Tikukulemberani zimenezi kuti chimwemwe chathu
chikhale chathunthu.

*Kuyenda mu Kuwunika*

5 Uthenga umene tinamva kwa Iye ndipo tikuwulalikira kwa inu ndi
uwu: Mulungu ndiye kuwunika ndipo mwa Iye mulibe mdima konse.
6 Tikanena kuti timayanjana naye, koma n'kumayendabe mu mdima,
tikunama ndipo sitikuchita choonadi. 7 Koma tikamayenda m'kuwunika,
monga Iye ali m'kuwunika, pamenepo timayanjana wina ndi mnzake,
ndipo magazi a Yesu, Mwana wake, amatitsuka ndi kutichotsera tchimo
lililonse.

*Kuwulula Machimo ndi Kukhululukidwa*

8 Tikanena kuti tilibe tchimo, tikudzinyenga tokha ndipo mwa ife mulibe
choonadi. 9 Koma tikavomereza machimo athu, Iye ndi wokhulupirika ndi
wolungama ndipo adzatikhululukira machimo athu, nadzatiyeretsa ndi
kutichotsera chosalungama chilichonse. 10 Ife tikanena kuti sitinachimwe,
tikumutenga Mulungu kukhala wonama, ndipo Mawu ake sali mwa ife.

## 2

1 Inu Ana anga okondedwa, ndikukulemberani zimenezi kuti
musachimwe. Koma wina akachimwa, tili nayo Nkhoswe yotinenera
kwa Atate, Yesu Khristu, Wolungamayo. 2 Iyeyo ndiye nsembe yopepesera
machimo athu, ndipo osati athu okha, komanso machimo onse a dziko
lapansi.

*Chikondi ndi Chidani*

3 Ife timatsimikiza kuti tikumudziwa ngati tikusunga malamulo ake.
4 Munthu akamanena kuti, "Ine ndimadziwa Mulungu," koma samvera
malamulo a Mulunguyo, ndi wabodza ameneyo ndipo mwa iye mulibe
choonadi. 5 Koma munthu aliyense akamvera mawu ake, ndiye kuti
chikondi cha Mulungu chafikadi penipeni mwa iyeyo. Pamenepo timat-
simikizadi kuti tili mwa Iye. 6 Aliyense amene amati amakhala mwa
Mulungu, ayenera kukhala moyo umene Yesu ankakhala.

7 Okondedwa, sindikukulemberani lamulo latsopano koma lakale lomwe
lija, limene munali nalo kuyambira pachiyambi. Lamulo la kalelo ndi
mawu amene munawamva kale. 8 Komabe ndi lamulo latsopano limene
ndikukulemberani. Choonadi chake chikuoneka mwa Yesu ndiponso mwa

inu, chifukwa mdima ukutha ndipo kuwunika kwenikweni kwayamba kale kuwala.
9 Aliyense amene amati ali m'kuwunika, koma n'kumadana ndi m'bale
wake ali mu mdima. 10 Aliyense amene amakonda m'bale wake amakha-
lanso m'kuwunika, ndipo mwa iye mulibe chokhumudwitsa. 11 Koma
aliyense wodana ndi m'bale wake ali mu mdima ndipo akuyenda mu mdima. Iyeyo sakudziwa kumene akupita, chifukwa mdima wamudetsa m'maso mwake.

12 Inu ana okondedwa, ndikukulemberani
popeza kuti machimo anu akhululukidwa chifukwa cha dzina la Yesu.
13 Inu abambo, ndikukulemberani
popeza kuti munamudziwa Iye amene analipo kuyambira pachiyambi.
Inu anyamata, ndikukulemberani
popeza kuti munagonjetsa woyipayo.
14 Ana okondedwa, ndikukulemberani
chifukwa mumawadziwa Atate.
Abambo, ndikukulemberani
chifukwa munamudziwa Iye amene analipo kuyambira pachiyambi.
Inu anyamata, ndikukulemberani
chifukwa ndinu amphamvu.
Mawu a Mulungu amakhala mwa inu
ndipo mumamugonjetsa woyipayo.

### *Musakonde Dziko Lapansi*

15 Musamakonde dziko lapansi kapena chilichonse cha dziko lapansi.
Ngati munthu wina aliyense akonda dziko lapansi, mwa iyeyo mulibe
chikondi chokonda Atate. 16 Pakuti zonse za m'dziko lapansi, zilakolako za
thupi, zinthu zimene maso amakhumbira ndiponso kuyandikira zinthu za
moyo uno, zonsezi sizichokera kwa Atate, koma ku dziko lapansi. 17 Dziko
lapansi likupita pamodzi ndi zilakolako zake, koma amene amachita chifuniro cha Mulungu amakhalapo mpaka muyaya.

### *Anthu Okana Khristu*

18 Ana anga, ino ndi nthawi yotsiriza, ndipo monga munamva kale kuti
anthu okana Khristu akubwera, ngakhale tsopano okana Khristu ambiri
afika kale. Zimenezi zikutisonyeza kuti ino ndi nthawi yotsiriza. 19 Anthu
amenewa anachoka pakati pathu, komatu sanali a m'gulu lathu. Pakuti akanakhala a m'gulu lathu, akanakhalabe nafe, koma kuchoka kwawo kunatisonyeza kuti sanali a m'gulu lathu.
20 Koma inu muli ndi kudzoza kochokera kwa Woyerayo, ndipo nonsenu
mukudziwa choonadi. 21 Sindikukulemberani chifukwa choti simudziwa
choonadi ayi, koma chifukwa choti mumadziwa choonadicho, ndipo
mukudziwanso kuti bodza silichokera pa choonadi. 22 Wabodzayo ndani?
Ndi munthu aliyense amene amanena kuti Yesu si Mpulumutsi. Munthu
woteroyo ndi wokana Khristu, ndiponso amakana Atate, ndi Mwana.
23 Aliyense wokana Mwana alibenso Atate. Wovomereza Mwana alinso ndi Atate.
24 Onetsetsani kuti zimene munazimva kuyambira pachiyambi
zikhalebe mwa inu. Ngati zikhala mwa inu, inunso mudzakhala
mwa Mwana ndiponso mwa Atate. 25 Ndipo chimene anatilonjeza
n'chimenechi: moyo wosatha.

26 Ine ndikukulemberani zimenezi kuti ndikuwuzeni za amene akufuna
kukusocheretsani. 27 Koma za inu, kudzoza kumene munalandira kwa
Khristu kuli mwa inu, ndipo sipafunika wina aliyense kuti akuphunzitseni.
Koma kudzozako kumakuphunzitsani zinthu zonse, ndipo popeza kudzoza
kwakeko n'koona osati konama, monga munaphunzira, khalani mwa
Iyeyo.

### *Ana a Mulungu*

28 Tsopano ana okondedwa, khalani mwa Yesu, kuti pamene adzaonek-
era, ife tidzakhale otsimikizika mu mtima ndi wopanda manyazi pamaso
pake akamadzabwera.
29 Popeza mukudziwa kuti Khristu ndi wolungama, choncho mukudzi-
wanso kuti aliyense amene amachita chilungamo ndi mwana wa Mulungu.

## 3

1 Taonani kukula kwake kwa chikondi chimene Atate anatikonda nacho,
kuti titchedwe ana a Mulungu! Ndipo n'chimene ife tili! N'chifukwa
chake dziko lapansi silitidziwa chifukwa silinamudziwe Iye. 2 Abale
okondedwa, tsopano ndife ana a Mulungu, ndipo sichinaoneke chimene
tidzakhala. Koma tikudziwa kuti Yesu akadzaonekera, tidzafanana naye,
pakuti tidzamuona Iyeyo monga momwe alili. 3 Aliyense amene ali ndi
chiyembekezo ichi mwa Iye adziyeretse yekha, monga Iye ali woyera.
4 Aliyense amene amachimwa amaphwanya lamulo; pakuti tchimo ndi
kuphwanya lamulo. 5 Koma inu mukudziwa kuti Yesu anabwera kuti adza-
chotse machimo athu. Ndipo mwa Iye mulibe tchimo. 6 Aliyense wokhala
mwa Khristu sachimwa. Aliyense amene amachimwa sanamuone kapena
kumudziwa.
7 Ana okondedwa, musalole kuti aliyense akusocheretseni. Munthu
amene amachita chilungamo ndi wolungama, monga Khristu ali wol-
ungama. 8 Iye amene amachimwa ndi wa Satana, chifukwa mdierekezi
wakhala akuchimwa kuyambira pa chiyambi. Mwana wa Mulungu
anaonekera kuti awononge ntchito za mdierekezi. 9 Aliyense amene ndi
mwana wa Mulungu, sachimwirachimwira, popeza mbewu ya Mulungu
ili mwa iye, sangathe kuchimwa, chifukwa ndi mwana wa Mulungu.
10 Mmenemu ndi mmene timadziwira ana a Mulungu ndi amene ali ana a
mdierekezi. Aliyense amene sachita chilungamo si mwana wa Mulungu;
ngakhalenso amene sakonda m'bale wake.

### *Kukondana Wina ndi Mnzake*

11 Uthenga umene munawumva kuyambira pachiyambi ndi uwu:
Tizikondana wina ndi mnzake. 12 Musakhale ngati Kaini, amene anali
wa woyipayo ndipo anapha m'bale wake. Nanga anamupha chifukwa
chiyani? Chifukwa zochita zake zinali zoyipa ndipo zochita za m'bale
wake zinali zolungama. 13 Abale anga, musadabwe ngati dziko lapansi
lidana nanu. 14 Ife tikudziwa kuti tinatuluka mu imfa ndi kulowa m'moyo,
chifukwa timakonda abale athu. Aliyense amene sakonda m'bale wake
akanali mu imfa. 15 Aliyense amene amadana ndi m'bale wake ndi
wakupha, ndipo inu mukudziwa kuti wopha anthu mwa iye mulibe moyo
wosatha.
16 Mmene timadziwira chikondi chenicheni ndi umu: Yesu anapereka
moyo wake chifukwa cha ife. Ndipo nafenso tiyenera kupereka miyoyo
yathu chifukwa cha abale athu. 17 Ngati wina ali ndi chuma ndipo n'kuona

m’bale wake akusowa, koma wosamvera chisoni, kodi mwa iyeyo muli
chikondi cha Mulungu? [18] Ana okondedwa, chikondi chathu chisakhale
cha pakamwa pokha koma cha ntchito zathu ndi m’choonadi. [19] Pamenepo
tidzadziwa kuti tili pa choonadi ndipo tidzakhala okhazikika mtima
pamaso pa Mulungu, [20] nthawi zonse pamene mtima wathu utitsutsa.
Pakuti Mulungu ndi wamkulu kuposa mitima yathu ndipo Iye amadziwa
zonse.

[21] Anzanga okondedwa, ngati mitima yathu sikutitsutsa, tili nako
kulimbika mtima pamaso pa Mulungu. [22] Ndipo timalandira chilichonse
chimene tichipempha kwa Iye, chifukwa timamvera malamulo ake ndi
kuchita zimene zimamukondweretsa. [23] Ndipo lamulo lake ndi ili:
kukhulupirira dzina la Mwana wake, Yesu Khristu, ndi kukondana wina
ndi mnzake monga Iye anatilamulira. [24] Iwo amene amamvera malamulo
ake amakhala mwa Iye, ndipo Iye amakhala mwa iwo. Ndipo mmenemu
ndi momwe timadziwira kuti Iye akukhala mwa ife. Timadziwa mwa
Mzimu Woyera amene anatipatsa.

# 4

*Kuyesa Mizimu*

[1] Anzanga okondedwa, musakhulupirire mzimu uliwonse, koma yesani
mizimu ngati ikuchokera kwa Mulungu, chifukwa aneneri onama ambiri
afalikira m’dziko lapansi. [2] Mungathe kuzindikira Mzimu wa Mulungu
motere: Mzimu uliwonse umene umavomereza kuti Yesu Khristu anab-
wera m’thupi, ndi wochokera kwa Mulungu, [3] koma mzimu uliwonse
umene suvomereza Yesu, siwochokera kwa Mulungu. Uwu ndi mzimu
wa wokana Khristu umene munawumva kuti ukubwera ndipo ngakhale
tsopano wabwera kale m’dziko lapansi.

[4] Inu ana okondedwa, ndinu ochokera kwa Mulungu ndipo mwawag-
onjetsa aneneri onyengawa, chifukwa Iye amene ali mwa inu ndi
wamkulu kuposa amene ali m’dziko lapansi. [5] Aneneri onyengawa
ndi ochokera m’dziko lapansi, n’chifukwa chake amayankhula za dziko
lapansi, ndipo dziko lapansi limawamvera. [6] Ife ndi ochokera kwa
Mulungu, ndipo aliyense amene amadziwa Mulungu amamvera zimene
timayankhula. Koma aliyense amene sachokera kwa Mulungu samvera
zimene timayankhula. Mmenemu ndiye mmene timasiyanitsira pakati pa
mzimu wachoonadi ndi Mzimu wachinyengo.

*Mulungu ndiye Chikondi*

[7] Anzanga okondedwa, tiyeni tikondane wina ndi mnzake, pakuti
chikondi chimachokera kwa Mulungu. Aliyense amene ali ndi chikondi
ndi mwana wa Mulungu ndipo amadziwa Mulungu. [8] Aliyense amene
alibe chikondi sadziwa Mulungu, chifukwa Mulungu ndiye chikondi.
[9] Mmene Mulungu anaonetsera chikondi chake pakati pathu ndi umu:
Iye anatumiza Mwana wake mmodzi yekha ku dziko lapansi kuti mwa
Iyeyo tikhale ndi moyo. [10] Chikondi ndi ichi: osati kuti ife ndife
amene tinamukonda Mulungu, koma kuti Iyeyo ndiye amene anatikonda
ndipo anatumiza Mwana wake kuti akhale nsembe yopepesera machimo
athu. [11] Anzanga okondedwa, popeza Mulungu anatikonda chotere,
ifenso tiyenera kukondana wina ndi mnzake. [12] Palibe amene anaonapo
Mulungu, koma tikakondana wina ndi mnzake, ndiye kuti Mulungu

amakhala mwa ife ndipo chikondi chake chafika pachimake penipeni mwa
ife.
[13] Ife tikudziwa kuti timakhala mwa Iye ndipo Iyeyo amakhala mwa
ife chifukwa anatipatsa Mzimu wake. [14] Ndipo taona ndipo tikuchitira
umboni, kuti Atate anatuma Mwana wake kuti akhale Mpulumutsi wa
dziko lapansi. [15] Ngati aliyense avomereza kuti Yesu ndi Mwana wa
Mulungu, Mulungu amakhala mwa iye ndipo iyeyo amakhala mwa
Mulungu. [16] Tikudziwa ndipo timadalira chikondi chimene Mulungu ali
nacho pa ife.
Mulungu ndiye chikondi. Aliyense amene amakhala moyo wachikondi,
ali mwa Mulungu ndipo Mulungu amakhala mwa iye. [17] Chikondi
chafika pachimake penipeni pakati pathu, kotero kuti pa tsiku lachiweruzo
tidzakhala olimba mtima chifukwa m'dziko lapansi moyo wathu uli ngati
wa Khristu. [18] Mulibe mantha m'chikondi. Koma chikondi ndi changwiro
chimachotsa mantha, chifukwa mantha amabwera chifukwa choopa
chilango. Munthu amene ali ndi mantha, chikondi chake sichangwiro.
[19] Ife timakonda Mulungu chifukwa ndiye anayamba kutikonda. [20] Ngati
wina anena kuti, "Ine ndimakonda Mulungu," koma namadana ndi m'bale
wake ndi wabodza ameneyo. Pakuti aliyense amene sakonda m'bale wake,
amene akumuona, sangathenso kukonda Mulungu amene sanamuone.
[21] Ndipo Iye anatipatsa lamulo lakuti: Aliyense amene amakonda Mulungu
ayenera kukondanso m'bale wake.

# 5

*Chikhulupiriro mwa Mwana wa Mulungu*

[1] Aliyense amene amakhulupirira kuti Yesu ndi Khristu, iyeyo ndi
mwana wa Mulungu, ndipo aliyense amene amakonda Atate amakon-
danso Mwana wake. [2] Chodziwira kuti timakonda ana a Mulungu
n'chakuti timakonda Mulungu ndi kusunga malamulo ake. [3] Pakuti
kukonda Mulungu ndiye kusunga malamulo ake. Ndipo malamulo
ake siwolemetsa, [4] chifukwa aliyense amene ndi mwana wa Mulungu
amagonjetsa dziko lapansi. Chikhulupiriro chathu ndicho timagonjetsera
dziko lapansi. [5] Ndani amagonjetsa dziko lapansi? Yekhayo amene
amakhulupirira kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu.
[6] Uyu ndiye anabwera mwa madzi ndi magazi, ndiye Yesu Khristu.
Sanabwere mwa madzi okha, koma mwa madzi ndi magazi. Ndipo ndi
Mzimu Woyera amene akuchitira umboni, chifukwa Mzimu Woyera ndi
choonadi. [7] Pakuti pali atatu amene amachitira umboni. [8] Mzimu Woyera,
madzi ndi magazi; ndipo atatu amavomerezana. [9] Timalandira umboni wa
anthu, koma umboni wa Mulungu ndi wopambana. Umboniwo ndi umene
anachitira Mwana wake. [10] Aliyense amene amakhulupirira Mwana
wa Mulungu ali nawo umboniwu mu mtima mwake, koma aliyense
amene sanakhulupirire Mulungu amayesa kuti Mulunguyo ndi wonama,
chifukwa sanakhulupirire umboni umene Mulungu anachitira wa Mwana
wake. [11] Ndipo umboniwo ndi uwu: Mulungu anatipatsa moyo wosatha,
ndipo moyowu uli mwa Mwana wake. [12] Iye amene ali ndi Mwana ali ndi
moyo, amene alibe Mwana wa Mulungu alibe moyo.

*Mawu Otsiriza*

[13] Ine ndikulemba zimenezi kwa inu, amene mwakhulupirira dzina la
Mwana wa Mulungu kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha. [14] Ife

timalimba mtima tikamafika pamaso pa Mulungu, popeza kuti ngati
tipempha kanthu kalikonse monga mwa chifuniro chake, amatimvera.
15 Ndipo ngati tikudziwa kuti amatimvera, chilichonse chimene timapem-
pha, tikudziwanso kuti tili nacho chimene tamupempha Iye.
16 Ngati wina aona m'bale wake akuchita tchimo losadzetsa imfa, apem-
phere ndipo Mulungu adzamupatsa moyo m'bale wakeyo. Ndikunena za
ochita tchimo losadzetsa imfa. Pali tchimo lodzetsa imfa. Ine sindikunena
kuti apemphere ayi. 17 Chilichonse chosalungama ndi tchimo ndipo pali
tchimo losadzetsa imfa.
18 Tikudziwa kuti aliyense amene ndi mwana wa Mulungu
sachimwirachimwirabe. Yesu, Mwana wa Mulungu, amamusunga ndipo
woyipa uja sangamukhudze. 19 Tikudziwa kuti ndife ana a Mulungu ndi
kuti dziko lonse lapansi lili pansi pa ulamuliro wa woyipayo. 20 Tikudziwa
kuti Mwana wa Mulungu anafika ndipo anatipatsa nzeru, kuti timudziwe
Iye amene ali woona. Ndipo ife tili mwa Iye amene ndi woona, Mwana
wake, Yesu Khristu. Iye ndi Mulungu woona ndi moyo wosatha.
21 Ana okondedwa, dzisungeni bwino, osapembedza mafano.

# KALATA YACHIWIRI YA YOHANE

1 Ndine mkulu wampingo, kulembera:
Mayi wosankhidwa ndi Mulungu ndi kwa ana ake amene ndi-
mawakonda m'choonadi. Ndipo sindine ndekha amene ndimawakonda,
komanso onse odziwa choonadi. 2 Timakukondani chifukwa cha choonadi
chimene chimakhala mwa ife ndipo chidzakhala mwa ife mpaka muyaya.
3 Chisomo, chifundo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate ndi
kwa Yesu Khristu, Mwana wa Atate, zikhale ndi ife m'choonadi ndi
m'chikondi.

*Choonadi ndi Chikondi*

4 Ndinakondwera kwambiri nditapeza ana anu ena akuyenda
m'choonadi, monga Atate anatilamulira. 5 Ndipo tsopano, amayi
wokondedwa, sindikukulemberani lamulo latsopano koma lomwe
lija takhala nalo kuyambira pachiyambi. Ine ndikukupemphani kuti
tidzikondana wina ndi mnzake. 6 Ndipo chikondi ndiye kuyenda momvera
malamulo ake. Lamulo lake ndi lakuti mukhale moyo wachikondi monga
munamva kuyambira pachiyambi.
7 Ndikunena zimenezi chifukwa anthu ambiri onyenga, amene
savomereza kuti Yesu Khristu anabwera monga munthu, akuyenda
m'dziko lapansi. Munthu aliyense otere ndi wonyenga ndiponso wokana
Khristu. 8 Chenjerani kuti mungataye chimene mwagwirira ntchito,
koma chitani khama kuti mukalandire mphotho yanu yonse. 9 Aliyense
amene sasunga chiphunzitso cha Khristu, alibe Mulungu. Koma amene
amasunga chiphunzitsochi, ameneyo alinso ndi Atate ndi Mwana. 10 Ngati
wina aliyense abwera kwa inu osaphunzitsa zimenezi, musamulandire
m'nyumba mwanu kapena kumupatsa moni. 11 Aliyense wolandira
munthu wotere ndiye kuti akuvomerezana nazo ntchito zake zoyipa.
12 Ndili nazo zambiri zoti ndikulembereni, koma sindikufuna kuzilemba
m'kalata. M'malo mwake, ndikuyembekeza kufika kwanuko kuti tidza-
kambirane nanu pamaso ndi pamaso, potero chimwemwe chathu chidza-
khala chathunthu.
13 Ana a mlongo wanu wosankhidwa ndi Mulungu akupereka moni.

# KALATA YACHITATU YA YOHANE

1 Ndine mkulu wampingo, kulembera:
Gayo mnzanga wokondedwa, amene ndimamukonda m'choonadi.

2 Wokondedwa, ndimakupempherera kuti zako zonse zikuyendere
bwino, ndikuti ukhale bwino m'thupi mwako, monga momwe ulili moyo
wako wauzimu. 3 Ine ndinali ndi chimwemwe chachikulu pamene abale
ena anafika n'kundifotokozera za kukhulupirika kwako pa choonadi
ndiponso mmene umayendera motsata choonadi. 4 Palibe chondikondw-
eretsa kwambiri kuposa kumva kuti ana anga akukhala m'choonadi.
5 Wokondedwa, ndiwe wokhulupirika pa zimene ukuchitira abale,
ngakhale kuti iwowo ndi alendo. 6 Iwo anafotokozera mpingo za chikondi
chako. Chonde uwathandize kupitiriza ulendo m'njira yokondweretsa Mu-
lungu. 7 Pakuti ananyamuka ulendo wawo chifukwa cha dzina la Ambuye,
osalandira thandizo kwa osakhulupirira. 8 Ife tiyenera kumathandiza
anthu oterewa, kuti tigwirizane nawo pa ntchito ya choonadi.

*Za Diotrefe ndi Demetriyo*

9 Ndinalembera mpingo, koma Diotrefe, amene amafuna kukhala
wotsogolera, sanafune kutimvera. 10 Tsono ndikabwera ndidzakumbutsa
zimene iye amachita. Iye amafalitsa nkhani zabodza zonena ife. Ndipo
sakhutira ndi zimenezo, komanso iyeyo amakana kulandira abale. Ko-
manso amaletsa amene akufuna kutero, ndipo amawachotsa mu mpingo.
11 Wokondedwa, usatsatire zinthu zoyipa koma zinthu zabwino.
Aliyense amene amachita zinthu zabwino ndi wochokera kwa Mulungu.
Aliyense amene amachita zoyipa sanamuonepo Mulungu. 12 Aliyense
akumuchitira umboni wabwino wa Demetriyo. Ngakhale choona chomwe
chimamuchitira umboni, ndipo iweyo ukudziwa kuti umboni wathu ndi
woona.
13 Ndili ndi zambiri zoti ndikulembereni, koma sindikufuna kuzilemba
m'kalata. 14 Ndiyembekezera kufika kwanuko posachedwapa, ndipo
tidzakambirana pamaso ndi pamaso.

15 Mtendere ukhale nawe. Abwenzi anu kuno akupereka moni. Upereke
moni kwa abwenzi onse mmodzimmodzi.

# KALATA YA YUDA

1 Ndine Yuda, mtumiki wa Yesu Khristu, komanso m'bale wake wa
Yakobo.

Kwa inu amene Mulungu Atate anakuyitanani, amene amakukondani
ndikukusungani mwa Yesu Khristu.

2 Chifundo, mtendere ndi chikondi zikhale nanu mochuluka.

## *Tchimo ndi Kuwonongeka kwa Osapembedza*

3 Okondedwa, ngakhale ndinkafunitsitsa kukulemberani za chipulu-
mutso cha tonsefe, ndakakamizidwa kuti ndikulembereni ndi kukupem-
phani kolimba kuti mumenye ndithu nkhondo yotchinjiriza chikhulupiriro
chimene Mulungu anachipereka kamodzi kokha kwa anthu onse oyera
mtima. 4 Pakuti anthu ena amene za chilango chawo zinalembedwa
kale, alowa mobisika pakati panu. Amenewa ndi anthu osapembedza
Mulungu, amene amapotoza chisomo cha Mulungu wathu kuchisandutsa
ufulu ochitira zonyansa ndiponso amakana Yesu Khristu amene Iye ndiye
Mbuye ndi Mfumu yathu.

5 Ngakhale munazidziwa kale zonsezi, ndafuna kuti ndikukumbutseni
kuti Ambuye anapulumutsa anthu ake ndi kuwatulutsa m'dziko la Igupto,
koma pambuyo pake anawononga amene sanakhulupirire. 6 Ndipo
mukumbukire angelo amene sanakhutire ndi maudindo awo, koma
anasiya malo awo. Angelo amenewa Mulungu anawamanga ndi maun-
yolo osatha, ndipo akuwasunga m'malo a mdima mpaka tsiku lalikulu
lachiweruzo. 7 Musayiwale mizinda ya Sodomu ndi Gomora ija, ndi
mizinda yoyandikana nayo. Anthu m'menemo anadziperekanso kuchita
zadama ndi kuchita zonyansa zachilendo. Mizinda imeneyi yakhala ngati
chitsanzo cha amene adzalangidwa ndi moto wosatha.

8 N'chimodzimodzinso zimene akuchita anthu amenewa potsata mal-
oto awo, amadetsa matupi awo, amakana ulamuliro wa Mulungu
ndiponso amachitira chipongwe angelo akumwamba. 9 Koma ngakhale
mkulu wa angelo Mikayeli, pamene ankalimbana ndi Mdierekezi za
mtembo wa Mose, sanamunene kuti wachipongwe, koma anati, "Ambuye
akudzudzule iwe!" 10 Koma anthu awa amachita chipongwe zinthu zimene
sakuzidziwa. Ndipo zinthu zimene amazidziwa ndi nzeru zachibadwa,
monga za nyama, ndizo zimene zimawawononga.

11 Tsoka kwa iwo chifukwa anatsatira njira ya Kaini. Iwo athamangira
phindu, n'chifukwa chake anagwa m'tchimo la Baalamu. Iwo ana-
wonongedwa chifukwa chowukira monga anachitira Kora.

12 Anthu amenewa ndiwo amayipitsa maphwando anu achikondi.
Amadya nanu mopanda manyazi ndipo ali ngati abusa amene aman-
godzidyetsa okha. Anthuwa ali ngati mitambo yowuluzika ndi mphepo,
yopanda mvula. Ali ngati mitengo ya nthawi ya masika, yopanda zipatso,
yozuka mizu, mitengo yoferatu. 13 Iwowa ali ngati mafunde awukali
apanyanja, amene amatulutsa thovu la zonyansa zawo. Amenewa ali ngati
nyenyezi zosochera, ndipo Mulungu akuwasungira mdima wandiweyani
mpaka muyaya.

14 Enoki, wachisanu ndi chiwiri kuyambira pa Adamu, ananeneratu
za anthu amenewa kuti, "Onani, Ambuye akubwera ndi oyera ake

osawerengeka [15] kuti adzaweruze aliyense, ndi kudzagamula kuti onse
osapembedza ndi olakwa, chifukwa cha ntchito zawo zosalungama zimene
anachita m'moyo wawo osaopa Mulungu. Adzawatsutsa chifukwa cha
mawu onse achipongwe amene osapembedzawa ananyoza nawo Am-
buye." [16] Anthu amenewa amang'ung'udza ndi kudandaula. Amatsatira
zilakolako zawo zoyipa. Amayankhula zodzitamandira ndipo amanamiza
ena pofuna kupeza phindu.

### *Awalimbikitsa kuti Apirire*

[17] Koma okondedwa, kumbukirani zimene atumwi a Ambuye athu
Yesu Khristu ananeneratu. [18] Iwo anakuwuzani kuti, "M'masiku otsiriza
kudzafika anthu onyoza, otsatira zofuna zawo zoyipa." [19] Anthu ame-
newa ndi amene akubweretsa mipatuko pakati panu, amatsatira nzeru
zachibadwa ndipo alibe Mzimu Woyera.

[20] Koma inu okondedwa, muthandizane kuti mukule pa chikhulupiriro
chanu choyera, ndipo muzipemphera ndi mphamvu ya Mzimu Woyera.
[21] Khalani m'chikondi cha Mulungu pamene mukudikira chifundo cha
Ambuye athu Yesu Khristu kuti akubweretsereni moyo wosatha.

[22] Muwachitire chifundo amene akukayika. [23] Ena muwapulumutse
powalanditsa ku moto. Enanso muwachitire chifundo, koma mwa
mantha, ndipo muzidana ngakhale ndi mwinjiro yomwe yayipitsidwa ndi
machimo.

### *Mawu Olemekeza Mulungu*

[24] Kwa Iye amene angathe kukusungani kuti mungagwe m'machimo,
ndiponso amene angathenso kukufikitsani pamaso pake pa ulemerero
wopanda cholakwa muli okondwa, [25] kwa Mulungu yekhayo, Mpulumutsi
wathu, kwa Iye kukhale ulemerero, ukulu, mphamvu ndi ulamuliro,
mwa Yesu Khristu Ambuye athu, kuyambira isanayambe nthawi, tsopano
mpaka muyaya. Ameni.

# CHIVUMBULUTSO
# CHA YESU KHRISTU KWA YOHANE

*Mawu Oyamba*

1 Vumbulutso lochokera kwa Yesu Khristu, limene Mulungu anamupatsa
kuti aonetse atumiki ake zimene zinayenera kuchitika posachedwa. Iye
anatuma mngelo wake kuti adziwitse mtumiki wake Yohane, 2 amene
akuchitira umboni chilichonse chimene anachiona. Awa ndi Mawu
a Mulungu ndi umboni wa Yesu Khristu. 3 Ngodala munthu amene
awerenga mawu oneneratu zam'tsogolo ndi iwo amene amamva ndi
kusunga zolembedwa m'bukuli pakuti nthawi yayandikira.

*Malonje kwa Mipingo Isanu ndi Iwiri*

4 Ndine Yohane,

Kupita ku mipingo isanu ndi iwiri ya m'chigawo cha Asiya.

Chisomo ndi mtendere kwa inu, kuchokera kwa Iye amene ali, amene
analipo ndi amene akubwera ndi kwa mizimu isanu ndi iwiri yokhala
patsogolo pa mpando wake waufumu, 5 ndiponso kuchokera kwa Yesu
Khristu mboni yokhulupirika, woyamba kuukitsidwa, ndi wolamulira
mafumu a dziko lapansi.

Kwa Iye amene amatikonda ndipo watimasula ku machimo athu ndi
magazi ake, 6 ndipo watisandutsa mafumu ndi ansembe kuti tizitumikira
Mulungu ndi Atate ake. Kwa Iye kukhale ulemerero ndi mphamvu ku
nthawi zosatha, Ameni.

7 "Onani akubwera ndi mitambo,"
ndipo "Aliyense adzamuona,
ndi amene anamubaya omwe."
Ndipo anthu a mitundu yonse ya pa dziko lapansi "adzalira
ching'ang'adza chifukwa cha Iye."
Zidzakhaladi momwemo, Ameni.

8 "Ine ndine Alefa ndi Omega," akutero Ambuye Mulungu Wamphamvu-
zonseyo "amene muli, amene munalipo, ndi amene mudzakhalapo."

*Wina Wokhala ngati Mwana wa Munthu*

9 Ine Yohane m'bale wanu ndi mnzanu m'masautso ndi mu ufumu ndi
mukupirira kwambiri, zomwe ndi zathu mwa Yesu, ndinali pa chilumba
cha Patimo chifukwa cha Mawu a Mulungu ndi umboni wa Yesu. 10 Pa
tsiku la Ambuye ndinanyamulidwa ndi Mzimu ndipo ndinamva kumbuyo
kwanga mawu ofuwula ngati lipenga, 11 amene anati, "Lemba m'buku
zimene ukuziona ndipo uzitumize ku mipingo isanu ndi iwiri ya ku Efeso,
Simurna, Pergamo, Tiyatira, Sarde, Filadefiya ndi ku Laodikaya."

12 Nditatembenuka kuti ndione amene amandiyankhulayo, ndinaona
zoyikapo nyale zisanu ndi ziwiri zagolide. 13 Pakati pa zoyikapo nyalezo
ndinaona wina wooneka ngati Mwana wa Munthu atavala mkanjo wofika
kumapazi ake ndipo anamangirira lamba wagolide pa chifuwa pake.
14 Tsitsi lake linali loyera ngati thonje, kuyera ngati matalala, ndipo maso
ake amawala ngati malawi amoto. 15 Mapazi ake anali ngati chitsulo choti
chili m'ng'anjo yamoto, ndipo mawu ake anali ngati mkokomo wamadzi
othamanga. 16 M'dzanja lake lamanja ananyamula nyenyezi zisanu ndi

ziwiri, ndipo m'kamwa mwake munali lupanga lakuthwa konsekonse.
Nkhope yake imawala ngati dzuwa lowala kwambiri.
17 Nditamuona ndinagwa pa mapazi ake ngati wakufa. Kenaka Iye
anasanjika dzanja lake lamanja pa ine nati, "Usachite mantha. Ndine
Woyamba ndi Wotsiriza. 18 Ine ndine Wamoyo; ndinali wakufa ndipo
taona ndine wamoyo mpaka muyaya! Ndipo ndili ndi makiyi a imfa ndi
Hade.
19 "Chomwecho, lemba zimene waona, zimene zilipo panopa ndi zimene
zidzachitike m'tsogolo. 20 Tanthauzo la nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimene
waziona m'dzanja langa lamanja ndi la zoyikapo nyale zagolide zisanu ndi
ziwiri ndi ili: Nyenyezi zisanu ndi ziwiri ndi angelo a mipingo isanu ndi
iwiri ija, ndipo zoyikapo nyale zisanu ndi ziwiri zija ndi mipingo isanu ndi
iwiri ija."

# 2

*Kalata Yolembera Mpingo wa ku Efeso*

1 "Lembera mngelo wa mpingo wa ku Efeso kuti:

Awa ndi mawu ochokera kwa amene ali ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri
zija m'dzanja lake lamanja amene akuyenda pakati pa zoyikapo nyale
zisanu ndi ziwiri zagolide. 2 Ine ndimadziwa zochita zako, ntchito yako
yowawa ndi kupirira kwako. Ine ndimadziwa kuti sungalekerere anthu
oyipa amene amadzitcha atumwi pamene sichoncho, unawayesa, ndipo
unawapeza kuti ndi abodza. 3 Iwe wapirira ndipo wakumana ndi zovuta
chifukwa cha dzina langa, ndipo sunatope.
4 Komabe ndili ndi chotsutsana nawe: Wataya chikondi chako
chapoyamba. 5 Kumbukirani kuti munagwa kuchokera patali. Lapa
ndikuchita zinthu zimene unkachita poyamba. Ngati sulapa ndidzab-
wera ndikukuchotsera choyikapo nyale chako pamalo pake. 6 Komabe
chokomera chako ndi chakuti umadana ndi zochita za Anikolai, zimene
Inenso ndimadana nazo.
7 Amene ali ndi makutu, amve zimene Mzimu akuwuza mipingo.
Amene adzapambana, ndidzamupatsa ufulu wakudya zipatso za mtengo
wopatsa moyo umene uli ku paradizo wa Mulungu.

*Kalata Yolembera Mpingo wa ku Simurna*

8 "Lembera mngelo wa mpingo wa ku Simurna kuti:

Awa ndi mawu ochokera kwa amene ndi Woyamba ndi Wotsiriza,
amene anafa n'kukhalanso ndi moyo. 9 Ine ndimadziwa masautso ako
ndi umphawi wako, chonsecho ndiwe wolemera! Ndikudziwa zimene
amakusinjirira anthu amene amati ndi Ayuda pamene sizili choncho,
koma ndi a mpingo wa Satana. 10 Musachite mantha ndi zimene
muti musauke nazo posachedwapa. Ndithu, Satana adzayika ena a
inu m'ndende pofuna kukuyesani, ndipo mudzazunzika kwa masiku
khumi. Khalani okhulupirika ngakhale zitafika pa imfa, ndipo Ine
ndidzakupatsani chipewa cha ulemerero wamoyo.
11 Amene ali ndi makutu, amve zimene Mzimu akuwuza mipingo.
Amene adzapambana sadzapwetekedwa ndi pang'ono pomwe ndi imfa
yachiwiri.

*Kalata Yolembera Mpingo wa ku Pergamo*

12 “Lembera mngelo wa mpingo wa ku Pergamo kuti:

Awa ndi mawu ochokera kwa amene ali ndi lupanga lakuthwa
konsekonse. 13 Iye akuti, ‘Ine ndimadziwa kumene mumakhala, kumene
kuli mpando waufumu wa Satana. Komabe inu ndinu okhulupirika
kwa Ine. Simunataye chikhulupiriro chanu pa Ine, ngakhale m’masiku
a Antipa, mboni yanga yokhulupirika, amene anaphedwa mu mzinda
wanu, kumene amakhala Satana.
14 Komabe, ndili ndi zinthu zingapo zotsutsana nanu. Kumeneko muli
ndi anthu ena amene amatsata ziphunzitso za Balaamu, uja amene ana-
phunzitsa Baraki kukopa Aisraeli kuti azidya nsembe zoperekedwa ku
mafano ndi kumachita chigololo. 15 Chimodzimodzinso inuyo muli ndi
ena amene amatsatira ziphunzitso za Anikolai. 16 Tsono tembenukani
mtima. Mukapanda kutero, ndidzabwera kwanuko posachedwa ndipo
ndidzachita nanu nkhondo ndi lupanga lotuluka m’kamwa mwanga lija.
17 Amene ali ndi makutu, amve zimene Mzimu akuwuza mipingo. Kwa
amene adzapambane ndidzamupatsa chakudya chobisika cha mana.
Ndidzamupatsanso mwala woyera wolembedwapo dzina latsopano,
lodziwa iye yekha amene walandirayo.’ ”

*Kalata Yolembera Mpingo wa ku Tiyatira*

18 “Lembera mngelo wampingo wa ku Tiyatira kuti:

Awa ndi mawu ochokera kwa Mwana wa Mulungu, amene maso ake
ali ngati moto woyaka ndi mapazi ake ngati chitsulo chonyezimira. 19 Iye
akuti: Ndimadziwa ntchito zanu, chikondi chanu ndi chikhulupiriro
chanu, kutumikira kwanu ndi kupirira kwanu. Ndikudziwa tsopano kuti
ntchito zanu ndi zabwino kuposa zoyamba zija.
20 Komabe ndili ndi chinthu chokudzudzula nacho. Umamulekerera
mkazi uja Yezebeli amene amadzitcha yekha kuti ndi mneneri. Iye ama-
phunzitsa atumiki anga kuti azichita zadama ndi kumadya zansembe
zoperekedwa ku mafano. 21 Ndamupatsa nthawi kuti aleke zachigololo
zake koma sakufuna. 22 Tsono ndidzamugwetsa m’masautso ndipo
amene amachita naye zadama zakezo ndidzawasautsa kwambiri aka-
panda kulapa ndi kuleka njira za mkaziyo. 23 Ana ake ndidzawakantha
ndi kuwapheratu. Kotero mipingo yonse idzadziwa kuti Ine ndine uja
amene ndimafufuza m’mitima mwa anthu ndi m’maganizo mwawo.
Aliyense wa inu ndidzachita naye monga mwa ntchito zake.
24 Tsopano ndikunena kwa enanu a ku Tiyatira, kwa inu amene
simunatsate chiphunzitso cha mkaziyo ndipo simunaphunzire zimene
iwo amati ndi ‘zinsinsi zonama’ za Satana. Kwa inu mawu anga ndi
akuti sindikuwunjikirani malamulo ena. 25 Inu mungogwiritsa zimene
munaphunzira basi, mpaka Ine ndidzabwere.
26 Amene adzapambana ndi kuchita chifuniro changa mpaka
kumapeto, ndidzamupatsa ulamuliro pa mitundu yonse ya anthu.
27 Adzayilamulira ndi ndodo yachitsulo ndipo nadzayiphwanyaphwanya
ngati mbiya. Ulamuliro umenewu ndi omwe ndinalandira kwa Atate
anga. 28 Ine ndidzamupatsanso nthanda, nyenyezi yowala m’mamawa
ija. 29 Amene ali ndi makutu, amve zimene Mzimu akuwuza mipingo.

# 3

*Kalata Yolembera Mpingo wa ku Sarde*

1 “Lembera mngelo wampingo wa ku Sarde kuti:

Awa ndi mawu ochokera kwa amene amasunga mizimu isanu ndi
iwiri ya Mulungu ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri. Iye akuti: Ndimadziwa
ntchito zako; umadziwika kuti ndiwe wamoyo koma ndiwe wakufa.
2 Dzuka! Limbitsa zimene zatsalira zomwe zatsala pang’ono kufa,
pakuti ndaona kuti ntchito zako n’zosakwanira pamaso pa Mulungu.
3 Choncho, kumbukira zimene unalandira ndi kumva; uzisunge ndipo
ulape. Koma ngati sudzuka, ndidzabwera ngati mbala ndipo sudzadziwa
nthawi imene ndidzabwere kwanu.
4 Komabe uli ndi anthu angapo mu Sarde amene sanadetse zovala
zawo. Amenewa adzayenda ndi Ine atavala zoyera popeza ndi
oyenera kutero. 5 Amene adzapambane adzavala zoyera ngati ena
aja. Sindidzafafaniza dzina lake m’buku lamoyo, koma ndidzamuchitira
umboni pamaso pa Atate anga ndi angelo ake. 6 Amene ali ndi makutu,
amve zimene Mzimu akuwuza mipingo.”

### *Kalata Yolembera Mpingo wa ku Filadefiya*

7 “Lembera mngelo wampingo wa ku Filadefiya kuti:

Awa ndi mawu ochokera kwa amene ndi woyera ndi woonadi, amene
ali ndi kiyi ya Davide. Iye akatsekula palibe amene angatseke; ndipo
akatseka palibe amene angatsekule. 8 Iye akuti, ‘Ine ndimadziwa ntchito
zako. Taona, ndakutsekulira pa khomo ndipo palibe wina amene
angatseke. Ndikudziwa kuti uli ndi mphamvu zochepa komabe wasunga
mawu anga ndipo sunandikane. 9 Amene ndi mpingo wa Satana, amene
amadzitcha kuti ndi Ayuda pamene sali choncho, koma ndi onama,
ndidzawabweretsa kwa inu ndi kuwagwetsa pansi pa mapazi anu kuti
adzazindikire kuti ndimakukondani. 10 Popeza mwasunga mawu anga
woti mupirire ndipo mwawugwira mtima, Inenso ndidzakupulumutsani
nthawi ya mayesero imene idzabwera pa dziko lonse lapansi kuyesa
onse okhala pa dziko lapansi.
11 Ine ndikubwera msanga. Gwiritsitsa chimene uli nacho kuti
wina angakulande chipewa chako chaufumu. 12 Iye amene adza-
pambane ndidzamusandutsa mzati wa m’Nyumba ya Mulungu wanga.
Sadzatulukamonso. Pa iye ndidzalemba dzina la Mulungu wanga ndi
dzina la mzinda wa Mulungu wanga, Yerusalemu watsopano, umene
ukubwera pansi kuchokera kumwamba kwa Mulungu wanga; ndipo pa
iye ndidzalembanso dzina langa latsopano. 13 Amene ali ndi makutu,
amve zimene Mzimu akuwuza mipingo.’ ”

### *Kalata Yolembera Mpingo wa ku Laodikaya*

14 “Lembera mngelo wampingo wa ku Laodikaya kuti:

Awa ndi mawu ochokera kwa Ameni, mboni yokhulupirika ndi
yoona, gwero la zolengedwa zonse za Mulungu. 15 Ine ndimadziwa
ntchito zako, kuti sindiwe wozizira kapena wotentha. Ndikanakonda
ukanakhala wozizira kapena wotentha! 16 Tsono popeza ndiwe wofunda
chabe, sindiwe wotentha kapena wozizira, ndatsala pang’ono kuti
ndikulavule m’kamwa mwanga. 17 Iwe umati: ‘Ndine wolemera,
ndine wachuma ndipo sindisowa kanthu.’ Koma sudziwa kuti ndiwe
wovutika, womvetsa chisoni, waumphawi, wosaona ndi wamaliseche.
18 Ndikukulangiza kuti ugule kwa Ine golide woyengedwa ndi moto

kuti ukhale wolemera. Ugule zovala zoyera kuti uvale ndi kuphimba
umaliseche wako wochititsa manyaziwo. Ndiponso ugule kwa Ine
mankhwala a m'maso kuti uwone.
19 Amene ndimawakonda ndimawadzudzula ndi kuwalanga. Choncho
chita changu ndipo lapa. 20 Taonani ndayima pa khomo ndikugogoda.
Ngati wina amva mawu anga natsekula chitseko, Ine ndidzalowamo ndi
kudya naye, Ine ndi iyeyo.
21 Amene adzapambana, ndidzamupatsa ufulu wokhala nane pamodzi
pa mpando wanga waufumu monga mmene Ine ndinapambana ndi
kukhala pansi ndi Atate anga pa mpando wawo waufumu. 22 Amene
ali ndi makutu, amve zimene Mzimu akuwuza mipingo."

# 4

### *Mapembedzedwe a Kumpando Waufumu Kumwamba*

1 Kenaka, nditayang'ana patsogolo panga ndinaona khomo lotsekuka la
kumwamba. Ndipo liwu lija ndinalimva poyamba lokhala ngati lipenga
linati, "Bwera kuno, ndipo ndidzakuonetsa zimene zichitike zikatha izi."
2 Nthawi yomweyo ndinatengedwa ndi Mzimu Woyera, ndipo patsogolo
panga ndinaona mpando waufumu wina atakhalapo. 3 Ndipo amene
anakhalapoyo anali wa maonekedwe ngati miyala ya jasipa ndi sardiyo.
Utawaleza wooneka ngati simaragido unazinga mpando waufumuwo.
4 Kuzungulira mpando waufumuwu panalinso mipando ina yaufumu
yokwana 24 ndipo panakhala akuluakulu 24 atavala zoyera ndipo anavala
zipewa zaufumu zagolide pamutu. 5 Kumpando waufumuwo kunkatuluka
mphenzi, phokoso ndi mabingu. Patsogolo pake pa mpando waufumuwo
panali nyale zisanu ndi ziwiri zoyaka. Iyi ndiyo mizimu isanu ndi iwiri
ya Mulungu. 6 Patsogolo pa mpando waufumu pomwepo panalinso ngati
nyanja yagalasi yonyezimira ngati mwala wa krustalo.

Pakatin'pakati, kuzungulira mpando waufumuwo panali zamoyo zi-
nayi zokhala ndi maso ponseponse, kutsogolo ndi kumbuyo komwe.
7 Chamoyo choyamba chinali ngati mkango, chachiwiri chinali ngati
mwana wang'ombe, chachitatu chinali ndi nkhope ngati munthu, chachi-
nayi chinali ngati chiwombankhanga chowuluka. 8 Chamoyo chilichonse
chinali ndi mapiko asanu ndi limodzi, ndipo chinali ndi maso ponseponse
ndi m'kati mwa mapiko momwe. Usana ndi usiku zimanena mosalekeza
kuti,

"Woyera, woyera, woyera
ndi Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse,
amene munali, amene muli ndi amene mukubwera."

9 Nthawi zonse zamoyozo zimapereka ulemerero, ulemu ndi mayamiko
kwa uja wokhala pa mpando waufumu, amene ali ndi moyo wamuyaya.
10 Izi zikamachitika akuluakulu 24 aja amadzigwetsa pansi pamaso pa
wokhala pa mpando waufumuyo, namupembedza wokhala ndi moyo
wamuyayayo. Iwo amaponya pansi zipewa zawo zaufumu patsogolo pa
mpando waufumu nati:

11 "Ndinu woyeneradi kulandira ulemerero ndi ulemu ndi mphamvu,
Ambuye ndi Mulungu wathu,
pakuti munalenga zinthu zonse,
ndipo mwakufuna kwanu
zinalengedwa monga zilili."

# 5

*Buku la Mwana Wankhosa*

[1] Kenaka ndinaona buku m'dzanja la wokhala pa mpando waufumu uja.
Bukulo linali lolembedwa mbali zonse ndipo linali lomatidwa ndi zomatira
zisanu ndi ziwiri. [2] Ndipo ndinaona mngelo wamphamvu akulengeza
ndi mawu okweza kuti, "Ndani ali woyenera kumatula zomatira ndi
kufutukula bukuli?" [3] Koma panalibe ndi mmodzi yemwe kumwamba
kapena pa dziko lapansi kapena kunsi kwa dziko lapansi woti afutukule
bukulo kapena kuona zam'kati mwake. [4] Ndinalira kwambiri chifukwa
panalibe amene anapezeka woyenera kufutukula bukuli kapena kuona
zam'kati mwake. [5] Tsono mmodzi mwa akuluakulu aja anati kwa
ine, "Usalire! Taona, Mkango wa fuko la Yuda, Muzu wa Davide,
wapambana. Iye angathe kufutukula bukuli ndi kumatula zomatira zisanu
ndi ziwirizo."

[6] Kenaka ndinaona Mwana Wankhosa akuoneka ngati wophedwa
atayimirira pakatikati pa mpando waufumu uja ndi zamoyo zinayi zija ndi
akuluakulu aja. Mwana Wankhosayo anali ndi nyanga zisanu ndi ziwiri
ndi maso asanu ndi awiri omwe ndi Mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu
yomwe anayitumiza ku dziko lonse lapansi. [7] Iye anabwera natenga buku
lija limene linali m'dzanja lamanja la wokhala pa mpando waufumuyo.
[8] Ndipo atalitenga, zamoyo zinayi zija ndi akuluakulu 24 aja anadzigwetsa
pansi pamaso pa Mwana Wankhosa. Aliyense wa akuluakuluwo anali
ndi zeze ndiponso mbale zagolide zodzaza ndi lubani. Lubaniyo ndi
mapemphero a oyera mtima. [9] Ndipo ankayimba nyimbo yatsopano
yakuti,

"Inu ndinu woyenera kulandira bukuli
ndi kumatula zomatira zake,
chifukwa munaphedwa,
ndipo magazi anu munagulira Mulungu
anthu a fuko lililonse, a chiyankhulo chilichonse, ndi mtundu uliwonse.
[10] Inu munawasandutsa kukhala mtundu waufumu ndi ansembe otumikira Mulungu,
ndipo adzalamulira dziko lapansi."

[11] Kenaka nditayang'ananso ndinamva mawu a angelo ambiri, miyan-
damiyanda kuchulukitsa ndi miyandamiyanda. Anazungulira mpando
waufumu pamodzi ndi zamoyo zija ndi akuluakulu aja. [12] Ndipo angelowo
anayimba ndi mawu ofuwula akuti,

"Mwana Wankhosa amene anaphedwayu
ndi woyenera kulandira ulamuliro, chuma, nzeru, mphamvu, ulemu,
ulemerero ndi mayamiko."

[13] Kenaka ndinamva mawu a cholengedwa chilichonse kumwamba, pa
dziko lapansi, kunsi kwa dziko lapansi, pa nyanja ndi zonse zili m'menemo
zikuyimba kuti,

"Kwa wokhala pa mpando waufumu ndi kwa Mwana Wankhosa,
kukhale mayamiko, ulemu, ulemerero ndi mphamvu
mpaka muyaya!"

[14] Zamoyo zinayi zija zinati: "Ameni," ndipo akuluakulu aja anadzigwetsa
pansi napembedza.

# 6

*Kutsekulidwa kwa Zimatiro Zisanu ndi Chimodzi*

1 Ndinaona pamene Mwana Wankhosa anatsekula chomatira choyamba
cha zomatira zisanu ndi ziwiri zija. Ndipo ndinamva chimodzi mwa
zamoyo zinayi zija chikunena liwu lomveka ngati bingu kuti, "Bwera!"
2 Nditayang'ana patsogolo pake ndinaona kavalo woyera! Wokwerapo
wake anali ndi uta ndipo anapatsidwa chipewa chaufumu, ndipo anatuluka kupita kukagonjetsa anthu ena.

3 Mwana Wankhosa atatsekula chomatira chachiwiri, ndinamva
chamoyo chachiwiri chija chikuti, "Bwera!" 4 Pamenepo kavalo wina
wofiira anatulukira. Wokwerapo wake anapatsidwa mphamvu yochotsa mtendere pa dziko lapansi ndi kuchititsa anthu kuti aziphana wina ndi mnzake. Iyeyu anapatsidwa lupanga lalikulu.

5 Mwana Wankhosa atatsekula chomatira chachitatu, ndinamva chamoyo chachitatu chikuti, "Bwera!" Nditayang'ana patsogolo panga ndinaona kavalo wakuda! Wokwerapo wake anali ndi masikelo awiri
m'manja mwake. 6 Ndinamva ngati liwu kuchokera pakati pa zamoyo
zinayi zija likuti, "Kilogalamu imodzi ya tirigu mtengo ndi malipiro a tsiku limodzi ndipo makilogalamu atatu a barele mtengo wake ndi malipiro a tsiku limodzi koma usawononge mafuta ndi vinyo!"

7 Mwana Wankhosa atatsekula chomatira chachinayi, ndinamva
chamoyo chachinayi chija chikunena kuti, "Bwera!" 8 Nditayang'ana
patsogolo panga ndinaona kavalo wotuwa! Wokwerapo wake dzina lake linali Imfa ndipo Hade inali kumutsatira pambuyo pake. Anapatsidwa ulamuliro pa gawo limodzi la magawo anayi a dziko lapansi kuti aphe ndi lupanga, njala, mliri, ndi zirombo zakuthengo za m'dziko lapansi.

9 Mwana Wankhosa atatsekula chomatira chachisanu, ndinaona kunsi
kwa guwa lansembe kunali mizimu ya anthu amene anaphedwa chifukwa
cha Mawu a Mulungu ndi chifukwa chochitira umboni. 10 Iwo anafuwula
kuti, "Mudzawaleka mpaka liti, Inu Ambuye wamkulu, woyera ndi woona, osawaweruza anthu okhala m'dziko lapansi ndi kulipsira magazi athu?"
11 Pamenepo aliyense wa anthuwo anapatsidwa mwinjiro woyera ndipo
anawuzidwa kuti adikire pang'ono kufikira chiwerengero cha anzawo ndi abale awo amene anayeneranso kuphedwa ngati iwo, chitakwanira.

12 Ndinayang'anitsitsa pamene ankatsekula chomatira chachisanu ndi
chimodzi. Ndipo panachitika chivomerezi champhamvu. Dzuwa linada ngati chiguduli chopanga ndi bweya wambuzi wakuda. Mwezi wonse
unafiira ngati magazi, 13 ndipo nyenyezi zakuthambo zinagwa pa dziko
lapansi ngati muja zimagwera nkhuyu zotsalira mu mtengo mphepo
yamphamvu ikawomba. 14 Thambo linachoka ngati amayalulira mphasa
ndipo phiri lililonse ndi chilumba chilichonse zinachotsedwa pa malo pake.

15 Kenaka, mafumu a pa dziko lapansi, ana a mafumu, atsogoleri
a ankhondo, olemera, amphamvu, kapolo aliyense, ndi mfulu aliyense
anakabisala kumapanga ndi pakati pa matanthwe a ku mapiri. 16 Iwo
anafuwulira mapiri ndi matanthwe kuti, "Tigwereni ndi kutivundikira kuti asatione wokhala pa mpando waufumuyo ndi kupulumuka ku
mkwiyo wa Mwana Wankhosa! 17 Pakuti tsiku lalikulu la mkwiyo wawo
lafika ndipo ndi ndani angathe kulimbapo?"

# 7

*Anthu 144,000*

1 Zitatha izi ndinaona angelo anayi atayima pa mbali zinayi za dziko
lapansi, atagwira mphepo zinayi za dziko lapansi kuletsa kuti mphepo
iliyonse isawombe pa dziko kapena pa nyanja kapena pa mtengo uliwonse.
2 Kenaka ndinaona mngelo wina akuchokera kummawa, ali ndi chidindo
cha Mulungu wamoyo. Iye anafuwulira angelo anayi aja amene anap-
atsidwa mphamvu yowononga dziko ndi nyanja kuti, 3 "Musawononge
dziko, nyanja ndi mitengo kufikira titalemba chizindikiro pa mphumi
za atumiki a Mulungu wathu." 4 Choncho ndinamva chiwerengero cha
amene ankayenera kulembedwa chizindikiro aja. Analipo okwanira
144,000 kuchokera ku mafuko onse a Israeli.

5 Ochokera fuko la Yuda analipo 12,000 amene analembedwa chizindikiro.
Ochokera fuko la Rubeni analipo 12,000;
ochokera fuko la Gadi analipo 12,000;
6 ochokera fuko la Aseri analipo 12,000;
ochokera fuko la Nafutali analipo 12,000;
ochokera fuko la Manase analipo 12,000;
7 ochokera fuko la Simeoni analipo 12,000;
ochokera fuko la Levi analipo 12,000;
ochokera fuko la Isakara analipo 12,000;
8 ochokera fuko la Zebuloni analipo 12,000;
ochokera fuko la Yosefe analipo 12,000;
ochokera fuko la Benjamini analipo 12,000.

*Gulu Lalikulu la Anthu Ovala Zoyera*

9 Zitatha izi ndinayang'ana patsogolo panga ndipo ndinaona gulu
lalikulu la anthu loti munthu sangathe kuliwerenga lochokera dziko
lililonse, fuko lililonse, mtundu wa anthu uliwonse ndi chiyankhulo
chilichonse, atayima patsogolo pa mpando waufumu, pamaso pa Mwana
Wankhosa. Iwo anali atavala mikanjo yoyera ndi kunyamula nthambi za
kanjedza m'manja mwawo. 10 Ndipo ankafuwula mokweza kuti:
"Chipulumutso chimachokera kwa Mulungu wathu,
wokhala pa mpando waufumu
ndi kwa Mwana Wankhosa."
11 "Angelo onse anayimirira kuzungulira mpando waufumu uja, kuzun-
guliranso akuluakulu aja ndi zamoyo zinayi zija. Angelo aja anadzigwetsa
pansi chafufumimba patsogolo pa mpando waufumu napembedza Mu-
lungu. 12 Iwo anati,
"Ameni!
Matamando ndi ulemerero,
nzeru, mayamiko, ulemu,
ulamuliro ndi mphamvu
zikhale kwa Mulungu wathu kunthawi zanthawi,
Ameni!"
13 Pamenepo mmodzi wa akuluakulu aja anandifunsa kuti, "Kodi avala
mikanjo yoyerawa ndani ndipo akuchokera kuti?"
14 Ine ndinayankha kuti, "Mbuye wanga mukudziwa ndinu."

Tsono iye anandiwuza kuti, “Amenewa ndi amene anatuluka
m’mazunzo aakulu aja. Anachapa mikanjo yawo naziyeretsa m’magazi
a Mwana Wankhosa. 15 N’chifukwa chake,
“iwowa ali patsogolo pa mpando waufumu wa Mulungu
ndipo akutumikira usana ndi usiku m’Nyumba ya Mulungu;
ndipo Iye wokhala pa mpando waufumu
adzawaphimba ndi tenti yake.
16 ‘Iwowa sadzamvanso njala,
sadzamvanso ludzu,
dzuwa kapena kutentha kulikonse
sikudzawawotcha.’
17 Pakuti Mwana Wankhosa amene ali pakati pa mpando waufumu
adzakhala m’busa wawo.
‘Iye adzawatsogolera ku akasupe a madzi amoyo.’
‘Ndipo Mulungu adzawapukuta misozi yonse m’maso mwawo.’ ”

# 8

### *Kutsekulidwa kwa Chimatiro Chachisanu ndi Chiwiri*

1 Atatsekula chomatira chachisanu ndi chiwiri, kumwamba kunakhala
chete mphindi makumi atatu.

2 Ndipo ndinaona angelo asanu ndi awiri aja amene amayimirira
pamaso pa Mulungu, akupatsidwa malipenga asanu ndi awiri.

3 Mngelo wina amene anali ndi chofukizira chagolide anabwera nay-
imirira pa guwa lansembe. Anapatsidwa lubani wambiri kuti amupereke
pamodzi ndi mapemphero a anthu onse oyera mtima pa guwa lansembe
lagolide patsogolo pa mpando waufumu. 4 Fungo la lubani pamodzi ndi
mapemphero a oyera mtima zinakwera kumwamba kwa Mulungu ku-
chokera m’dzanja la mngeloyo. 5 Kenaka mngeloyo anatenga chofukizira
nachidzaza ndi moto wochokera pa guwa lansembe ndi kuponya pa dziko
lapansi ndipo nthawi yomweyo panachitika mabingu, phokoso, mphenzi
ndi chivomerezi.

### *Malipenga*

6 Angelo asanu ndi awiri anakonzekera kuyimba malipenga asanu ndi
awiri.

7 Mngelo woyamba anayimba lipenga lake ndipo kunabwera matalala
ndi moto wosakanizana ndi magazi ndipo unaponyedwa pa dziko lapansi.
Gawo limodzi la magawo atatu a dziko lapansi linapsa, gawo limodzi la
magawo atatu a mitengo linapsa ndi gawo limodzi la magawo atatu a udzu
wauwisi linapsanso.

8 Mngelo wachiwiri anayimba lipenga lake, ndipo chinthu china
chooneka ngati phiri lalikulu loyaka moto, chinaponyedwa m’nyanja.
Gawo limodzi la magawo atatu a nyanja linasanduka magazi. 9 Gawo
limodzi mwa magawo atatu a zolengedwa zonse zamoyo za m’nyanja,
linafa, ndipo gawo limodzi la sitima za pamadzi linawonongedwa.

10 Mngelo wachitatu anayimba lipenga lake, ndipo nyenyezi yayikulu,
yoyaka ngati muni inachoka kumwamba nigwera pa gawo limodzi la
magawo atatu a mitsinje ndi pa akasupe amadzi. 11 Dzina la nyenyeziyo
ndi Chowawa. Gawo limodzi la magawo atatu a madzi anasanduka owawa
ndipo anthu ambiri anafa chifukwa cha madzi owawawo.

12 Mngelo wachinayi anayimba lipenga lake, ndipo chimodzi cha zigawo
zitatu za dzuwa, za mwezi ndi za nyenyezi zinamenyedwa kotero chimodzi

mwa zitatu za zonsezi zinada. Panalibenso kuwala pa chimodzi mwa zigawo zitatu za usana, ndi chimodzimodzinso usiku.

13 Ndinayang'ananso ndipo ndinaona ndi kumva chiwombankhanga chimene chinkawuluka mlengalenga kwambiri chikuyankhula mofuwula kuti, "Tsoka, Tsoka! Tsoka lalikulu kwa anthu okhala m'dziko lapansi, angelo otsala aja akangoyimba malipenga awo!"

# 9

1 Mngelo wachisanu anayimba lipenga lake, ndipo ndinaona nyenyezi
ikugwa pa dziko lapansi kuchokera ku thambo. Nyenyeziyo inapatsidwa
kiyi ya ku chidzenje chakuya. 2 Nyenyeziyo itatsekula pa chidzenje
chakuyacho panatuluka utsi ngati wochokera m'ng'anjo yayikulu. Dzuwa
ndi thambo zinada chifukwa cha utsi ochokera m'dzenjemo. 3 Ndipo
m'kati mwa utsimo munatuluka dzombe kukalowa m'dziko lapansi ndipo
linapatsidwa mphamvu zoluma ngati za zinkhanira pa dziko lapansi.
4 Dzombelo linalamulidwa kuti lisawononge udzu wa pa dziko lapansi,
kapena chomera chilichonse, kapena mtengo uliwonse, koma anthu
okhawo amene analibe chizindikiro cha Mulungu pa mphumi zawo.
5 Silinapatsidwe mphamvu yowapha koma yowazunza kwa miyezi isanu.
Ndipo ululu umene anthuwo anawumva unali ngati wa chinkhanira
chikaluma munthu. 6 Masiku amenewo anthu adzafunafuna imfa koma
sadzayipeza. Adzalakalaka kufa koma imfa izidzawathawa.

7 Dzombe linkaoneka ngati akavalo okonzekera nkhondo. Pamitu pawo
panali ngati zipewa zaufumu zagolide ndipo nkhope zawo ngati za anthu.
8 Tsitsi lawo linali ngati la amayi, mano awo ngati a mikango. 9 Dzombelo
linavala za pachifuwa zachitsulo. Phokoso la mapiko awo linali ngati
phokoso la magaleta ankhondo ambiri okokedwa ndi akavalo othamangira
ku nkhondo. 10 Linali ndi michira ngati zinkhanira ndi mbola. M'michira
yake munali mphamvu yozunza nayo anthu kwa miyezi isanu. 11 Mfumu
yawo inali mngelo wolamulira Chidzenje chakuya chija. M'chihebri dzina
lake ndi Abadoni ndipo m'Chigriki ndi Apoliyoni (tanthauzo lake ndiye
kuti, Wowononga).

12 Tsoka loyamba lapita; matsoka ena awiri akubwerabe.

13 Mngelo wachisanu ndi chimodzi anayimba lipenga lake, ndipo
ndinamva liwu lochokera ku ngodya zinayi za guwa lansembe lagolide
lija lokhala pamaso pa Mulungu. 14 Liwulo linati kwa mngelo wachisanu
ndi chimodzi amene anali ndi lipenga uja, "Masula angelo anayi amene
anamangidwa pa mtsinje waukulu wa Yufurate." 15 Ndipo anamasulid-
wadi angelo anayi aja amene anasungidwa kukonzekera ora ili, tsiku ili,
mwezi uwu ndi chaka ichi kuti aphe limodzi la magawo atatu a anthu.
16 Ndinamva chiwerengero cha ankhondo a pa akavalo aja, kuti chinali
200 miliyoni.

17 Akavalo ndi okwerapo amene ndinaona m'masomphenya anga
ankaoneka motere: Zovala za pachifukwa pawo zinali zofiira ngati moto,
zobiriwira ngati utsi, ndi zachikasu ngati miyala ya sulufule. Mitu ya
akavalowo inali ngati ya mikango ndipo m'kamwa mwawo munkatuluka
moto, utsi ndi sulufule. 18 Gawo limodzi la magawo atatu a anthu
linaphedwa ndi miliri yamoto, utsi ndi sulufule zimene zinkachoka
m'kamwa mwawo. 19 Mphamvu za akavalowo inali m'kamwa mwawo
ndi m'michira mwawo; pakuti michira yawo inali ngati njoka; ndi mitu
imene inkalumira.

[20] Anthu ena onse amene sanaphedwe ndi miliri imeneyi sanalapebe
kuti asiye ntchito zawo zoyipa. Iwo sanasiye kupembedza ziwanda ndi
mafano agolide, asiliva, amkuwa, amwala ndi amtengo, mafano amene
sangathe kuona, kumva kapena kuyankhula. [21] Sanalapenso kuleka
zakupha, zamatsenga awo, zachigololo zawo kapena umbava wawo.

# 10

*Mngelo ndi Kabuku*

[1] Kenaka ndinaona mngelo wina wamphamvu akutsika kuchokera
kumwamba. Anavala mtambo ndipo anali ndi utawaleza pamutu pake.
Nkhope yake inali ngati dzuwa, ndipo miyendo yake inali ngati mizati
yamoto. [2] M'dzanja lake munali kabuku kakang'ono kotsekulidwa.
Phazi lake lamanja linaponda m'nyanja ndipo phazi lake lamanzere
linaponda pa mtunda. [3] Mngeloyo anafuwula kwambiri ngati kubangula
kwa mkango. Atangofuwula, kunamveka kugunda kwa mabingu asanu
ndi awiri. [4] Mabingu asanu ndi awiriwo atangogunda, ine ndinkati
ndizilemba; koma ndinamva mawu kuchokera kumwamba kuti, "Zisunge
mu mtima zimene mabingu asanu ndi awiriwo anena ndipo usazilembe."

[5] Kenaka mngelo amene ndinamuona ataponda m'nyanja ndi ku
mtunda uja, anakweza dzanja lake lamanja kumwamba. [6] Mngeloyo
analumbira m'dzina la Iye wokhala ndi moyo mpaka muyaya, amene
analenga kumwamba ndi zonse zili kumeneko, dziko lapansi ndi zonse
zili m'menemo, nyanja ndi zonse zili m'menemo, nati, "Pasakhalenso
zochedwa tsopano! [7] Koma patsala pang'ono kuti mngelo wachisanu ndi
chiwiri uja awombe lipenga lake, chinsinsi cha Mulungu chidzachitika
monga momwe analengezera kwa atumiki ake, aneneri."

[8] Pamenepo mawu amene ndinamva kuchokera kumwamba aja,
anandiyankhulanso, anati, "Pita katenge buku lotsekulidwalo m'dzanja
la mngelo amene waponda pa nyanja ndi pa mtundayo."

[9] Choncho ndinapita kwa mngeloyo ndipo ndinamupempha kuti andi-
patse kabukuko. Iye anati, "Tenga, idya. M'mimba mwako kaziwawa
koma m'kamwa mwako kazizuna ngati uchi." [10] Ndinatenga kabukuko
m'dzanja la mngeloyo ndipo ndinadyadi. M'kamwa mwanga kankazuna
ngati uchi, koma nditakameza, m'mimbamu munkawawa. [11] Ndipo
anandiwuza kuti, "Iwe uyenera kulalikiranso za mitundu yambiri ya
anthu, za mayiko, ziyankhulo ndi za mafumu."

# 11

*Mboni Ziwiri*

[1] Ndinapatsidwa bango longa ndodo yoyezera ndipo ndinawuzidwa kuti,
"Pita, kayeze Nyumba ya Mulungu ndi guwa lansembe, ndipo ukawerenge
anthu opembedza m'Nyumbamo. [2] Koma bwalo lakunja ulisiye, usaliyeze
chifukwa linaperekedwa kwa a mitundu ina. Iwo adzawupondereza
mzinda woyerawo kwa miyezi 42. [3] Ndipo ndidzapereka mphamvu kwa
mboni zanga ziwiri, zitavala ziguduli, ndipo kwa masiku 1,260 zidzakhala
zikulalikira." [4] Mboni ziwirizo ndi mitengo iwiri ya olivi ndi zoyikapo
nyale ziwiri zija zimene zili pamaso pa Ambuye wa dziko lapansi. [5] Ngati
wina atafuna kuzipweteka mbonizo, moto umatuluka m'kamwa mwawo
ndikuwononga adani awo. [6] Mbonizo zili ndi mphamvu yomanga mvula
kuti isagwe pa nthawi imene akulalikirayo; ndipo zili ndi mphamvu

yosanduliza madzi kukhala magazi ndi yokantha dziko lapansi ndi miliri
ya mitundumitundu nthawi iliyonse imene zingafune.
7 Tsono zikadzatsiriza umboni wawowo, chirombo chotuluka
m'Chidzenje chakuya chija chidzachita nawo nkhondo n'kuzigonjetsa
mpaka kuzipha. 8 Mitembo yawo idzakhala ili gone pabwalo la mu
mzinda waukulu umene mozimbayitsa umatchedwa Sodomu ndi
Igupto, kumenenso Ambuye wawo anapachikidwako. 9 Kwa masiku
atatu ndi theka, anthu ochokera ku mtundu uliwonse, fuko lililonse,
chiyankhulo chilichonse ndi dziko lililonse, azidzayang'anitsitsa mitembo
yawoyo koma adzakana kuyikwirira. 10 Anthu okhala pa dziko lapansi
adzasangalala nazo zimenezi. Adzachita chikondwerero ndi kutumizirana
mphatso, chifukwa aneneri awiri amenewa ankasautsa anthu okhala pa
dziko lapansi.
11 Koma patapita masiku atatu ndi theka aja, mpweya wopatsa moyo
wochoka kwa Mulungu unalowa mwa aneneriwo, ndipo anayimirira,
ndipo amene anawaona anachita mantha aakulu. 12 Kenaka aneneri aja
anamva mawu ofuwula ochokera kumwamba owawuza kuti, "Bwerani
kuno." Ndipo anapitadi kumwamba mu mtambo adani awo aja akuwaona.
13 Nthawi yomweyo panachitika chivomerezi choopsa mwakuti chi-
gawo chimodzi cha magawo khumi a mzinda chinagwa. Anthu 7,000
anaphedwa ndi chivomerezicho, ndipo opulumukawo anachita mantha
kwambiri nayamba kutamanda Mulungu wakumwamba.
14 Tsoka lachiwiri lapita; koma tsoka lachitatu likubwera posachedwapa.

### *Lipenga Lachisanu ndi Chiwiri*

15 Mngelo wachisanu ndi chiwiri anawomba lipenga lake, ndipo
kumwamba kunamveka mawu ofuwula amene anati,

"Ufumu wa dziko lapansi uli
m'manja mwa Ambuye athu ndi Khristu wake uja,
ndipo adzalamulira mpaka muyaya."

16 Ndipo akuluakulu 24 aja okhala pa mipando yawo yaufumu pamaso
pa Mulungu, anadzigwetsa chafufumimba napembedza Mulungu 17 Iwo
anati,

"Ife tikuyamika Inu Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse,
amene mulipo ndipo munalipo,
chifukwa mwaonetsa mphamvu yanu yayikulu,
ndipo mwayamba kulamulira.
18 A mitundu ina anapsa mtima;
koma yafika nthawi yoonetsa mkwiyo.
Nthawi yakwana yoweruza anthu akufa,
yopereka mphotho kwa atumiki anu, aneneri,
anthu oyera mtima anu ndi amene amaopa dzina lanu,
wamng'ono pamodzi ndi wamkulu yemwe.
Yafika nthawi yowononga amene awononga dziko lapansi."

19 Pamenepo anatsekula Nyumba ya Mulungu kumwamba ndipo m'kati
mwake munaoneka Bokosi la Chipangano. Kenaka kunachita mphenzi,
phokoso, mabingu, chivomerezi ndipo kunachita mkuntho wamatalala
akuluakulu.

## 12

### *Mayi ndi Chinjoka*

1 Chizindikiro chachikulu chinaoneka kuthambo; mayi atavala dzuwa,
mapazi ake ataponda mwezi, pamutu pake pali chipewa chaufumu
chokhala ndi nyenyezi khumi ndi ziwiri. 2 Mayiyo anali woyembekezera
ndipo pa nthawi yake yochira analira mokuwa chifukwa cha ululu
wakubala. 3 Kenaka ku thambo kunaonekanso chizindikiro china;
chinjoka chachikulu kwambiri, chofiira chomwe chinali ndi mitu isanu ndi
iwiri ndi nyanga khumi; pamutu uliwonse chitavala chipewa chaufumu.
4 Mchira wake unakokolola gawo limodzi la magawo atatu a nyenyezi
kuzichotsa ku thambo ndi kuziponya pa dziko lapansi. Chinjoka chija
chinadzayima patsogolo pa mayi uja amene anali pafupi kuberekayu
kuti mwanayo akangobadwa chimudye. 5 Mayiyo anabereka mwana
wamwamuna amene adzalamulira anthu a mitundu ina yonse ndi ndodo
yachitsulo. Ndipo mwanayo analandidwa ku dzanja la mayiyo ndi kupita
naye kwa Mulungu ku mpando wake waufumu. 6 Mayiyo anathawira ku
chipululu ku malo kumene Mulungu anamukonzera, kumene akasamalid-
weko masiku 1,260.

7 Zitatero, kumwamba kunayambika nkhondo. Mikayeli ndi angelo ake
kumenyana ndi chinjoka chija. Chinjokacho ndi angelo ake anabwezer-
anso. 8 Koma analibe mphamvu ndipo anagonjetsedwa nathamangitsidwa
kumwambako. 9 Chinjoka chachikulu chija chinagwetsedwa pansi.
Ichocho ndiye njoka yakalekale ija yotchedwa Mdierekezi kapena Satana,
amene amasocheretsa anthu a pa dziko lonse lapansi. Chinaponyedwa pa
dziko la pansi pamodzi ndi angelo ake.

10 Kenaka ndinamva mawu ofuwula kumwamba akunena kuti,

“Tsopano chipulumutso, mphamvu,
ufumu wa Mulungu wathu
ndi ulamuliro wa Khristu wake zabwera.
Pakuti woneneza abale athu uja,
amene amangokhalira kuwaneneza pamaso pa Mulungu usana ndi usiku,
wagwetsedwa pansi.
11 Abale athuwo anamugonjetsa
ndi magazi a Mwana Wankhosa
ndiponso mawu a umboni wawo.
Iwo anadzipereka kwathunthu,
moti sanakonde miyoyo yawo.
12 Choncho, kondwerani, inu dziko lakumwamba
ndi onse okhala kumeneko!
Koma tsoka dziko lapansi ndi nyanja
chifukwa Mdierekezi wagwetsedwa kwa inu!
Iye wadzazidwa ndi ukali
chifukwa akudziwa kuti nthawi yake ndi yochepa.”

13 Pamene chinjokacho chinaona kuti chagwetsedwa pa dziko la-
pansi, chinayamba kuthamangitsa mayi uja amene anali atabala mwana
wamwamunayu. 14 Mayiyo anapatsidwa mapiko awiri a chiwom-
bankhanga chachikulu kuti athawire ku malo ake aja a ku chipululu.
Kumeneko adzasamalidwako zaka zitatu ndi theka kuti chinjoka chija
chisamupeze. 15 Kenaka chinjoka chija chinalavulira mayiyo madzi
ambiri ngati mtsinje, kuti madziwo amukokolole. 16 Koma dziko lapansi
linamuthandiza mayiyo. Nthaka inatsekuka ndi kumeza mtsinje uja
unachokera m’kamwa mwa chinjokacho. 17 Pamenepo chinjokacho
chinamupsera mtima mayiyo ndipo chinachoka kupita kukachita nkhondo

ndi ana ena onse a mayiyo, ndiye kuti anthu amene anasunga malamulo
a Mulungu ndi kuchitira umboni za Yesu.
18 Kenaka ndinaona chinjokacho chitayima m'mbali mwa nyanja.

# 13

*Chirombo Chotuluka M'nyanja*

1 Ndipo ndinaona chirombo chikutuluka m'nyanja. Chinali ndi nyanga
khumi ndi mitu isanu ndi iwiri. Pa nyanga iliyonse chinavala chipewa
chaufumu, ndipo pa mutu uliwonse panali dzina lonyoza Mulungu.
2 Chirombo chimene ndinachionacho chinali ngati kambuku, mapazi ake
ngati chimbalangondo, kukamwa kwake ngati kwa mkango. Chinjoka
chija chinapatsa chirombocho mphamvu zake, mpando wake waufumu
ndiponso ulamuliro waukulu. 3 Umodzi wa mitu wa chirombocho
unkaoneka ngati uli ndi bala losati n'kupola, koma n'kuti balalo litap-
ola. Dziko lonse linadabwa ndipo linatsatira chirombocho. 4 Anthu
anapembedza chinjoka chija chifukwa chinapereka ulamuliro wake kwa
chirombocho. Nachonso chirombo chija anachipembedza n'kumafunsa
kuti, "Ndani angafanane ndi chirombochi? Ndani angachite nacho
nkhondo?"
5 Chirombo chija chinaloledwa kuyankhula mawu onyada ndi
achipongwe kwa Mulungu. Chinapatsidwa mphamvu zolamulira pa
miyezi 42. 6 Ndipo chinayamba kuyankhula mawu achipongwe ony-
oza Mulungu, dzina lake, malo okhalamo ndi onse amene amakhala
kumwamba. 7 Chinaloledwa kuchita nkhondo ndi oyera mtima ndi
kuwagonjetsa. Ndipo chinapatsidwanso mphamvu zolamulira anthu a
fuko lililonse, mtundu uliwonse ndi chiyankhulo chilichonse. 8 Anthu
onse okhala pa dziko lapansi adzapembedza chirombocho, aliyense amene
chilengedwere cha dziko lapansi dzina lake silinalembedwe m'buku la
amoyo la Mwana Wankhosa anaphedwa uja.
9 Iye amene ali ndi makutu, amve.

10 "Woyenera kupita ku ukapolo,
adzapita ku ukapolo.
Woyenera kufa ndi lupanga,
adzafa ndi lupanga."

Pamenepa kwa anthu a Mulungu pakufunika kupirira ndi kukhulupirika.

*Chirombo Chotuluka M'nthaka*

11 Kenaka ndinaona chirombo china chikutuluka m'nthaka. Chinali
ndi nyanga ziwiri ngati mwana wankhosa koma kuyankhula kwake ngati
chinjoka. 12 Chinalamulira ndi mphamvu zonse za chirombo choyamba
chija, ndipo chinachititsa kuti dziko lapansi ndi anthu okhalamo alambire
chirombo choyamba chija, chimene bala lake losati n'kupola linali litapola.
13 Ndipo chinachita zizindikiro zazikulu zodabwitsa, mpaka kumagwetsa
moto pa dziko lapansi kuchokera kumwamba anthu akuona. 14 Chifukwa
cha zizindikiro zimene chinaloledwa kuchita m'malo mwa chirombo
choyamba chija, chimene bala lake linapola, chinanyenga anthu okhala
pa dziko lapansi. Chinalamula anthu kuti apange fano mopereka ulemu
kwa chirombo chimene chinavulazidwa ndi lupanga, koma n'kukhalabe
ndi moyo. 15 Chirombo cha chiwirichi chinapatsidwa mphamvu zaku-
pereka mpweya kwa fano la chirombo choyamba chija kuti liyankhule
ndi kuphetsa aliyense wokana kupembedza fanolo. 16 Chinakakamiza

aliyense, wamng'ono, wamkulu, wolemera, wosauka, mfulu ndi kapolo
kuti alembedwe chizindikiro pa dzanja lamanja kapena pa mphumi.
17 Chinkachita zimenezi kuti wina aliyense asaloledwe kugula kapena
kugulitsa kanthu ngati alibe chizindikiro chimenechi, chimene ndi dzina
la chirombocho kapena nambala yotanthauza dzina lake.

18 Pano pafunika nzeru. Munthu amene ali ndi nzeru atanthauze nam-
bala ya chirombocho, pakuti nambalayo ikutanthauza munthu. Nambala
yake ndi 666.

# 14

*Mwana Wankhosa ndi Anthu 144,000*

1 Kenaka ndinaona patsogolo panga panali Mwana Wankhosa, atay-
imirira pa Phiri la Ziyoni, ndipo Iye anali pamodzi ndi anthu 144,000
amene pa mphumi pawo panalembedwa dzina la Mwana Wankhosayo
ndi la Atate ake. 2 Ndipo ndinamva liwu lochokera kumwamba ngati
mkokomo wa madzi ambiri, ndiponso ngati kugunda kwamphamvu kwa
bingu. Liwu limene ndinamvalo linali ngati a anthu akuyimba azeze awo.
3 Anthuwo ankayimba nyimbo yatsopano patsogolo pa mpando waufumu
ndi zamoyo zinayi zija ndi akuluakulu aja. Palibe ndi mmodzi yemwe
amene anatha kuphunzira nyimboyo kupatula anthu 144,000 aja amene
anawomboledwa pa dziko lapansi. 4 Awa ndiwo amene sanadzidetse
koma anadzisunga ndipo sanadziyipitse ndi akazi. Anthu amenewa
ndiwo ankatsatira Mwana Wankhosa kulikonse kumene ankapita. Ndiwo
amene anagulidwa pakati pa anthu a dziko lapansi kuti akhale oyambirira
kuperekedwa kwa Mulungu ndi kwa Mwana Wankhosa. 5 Iwo sananenepo
bodza ndipo alibe cholakwa.

*Angelo Atatu*

6 Kenaka ndinaona mngelo wina akuwuluka mu mlengalenga ndipo
anali ndi Uthenga Wabwino wamuyaya woti akalalikire kwa anthu okhala
pa dziko lapansi, kwa a mtundu uliwonse, a fuko lililonse, a chiyankhulo
chilichonse ndi kwa anthu onse. 7 Mngeloyo anayankhula mokweza mawu
kuti, "Wopani Mulungu ndi kumutamanda, chifukwa nthawi yoweruza
anthu yafika. Mumupembedze Iye amene analenga thambo, dziko lapansi,
nyanja ndi akasupe amadzi."

8 Mngelo wachiwiri anatsatana naye ndipo anati, "Wagwa! Wagwa
Babuloni womveka uja, amene anachititsa anthu a mitundu yonse kumwa
vinyo wa zilakolako zake zachigololo."

9 Mngelo wachitatu anatsatana nawo ndi mawu ofuwula anati,
"Ngati wina apembedza chirombo chija ndi fano lake ndi kulembedwa
chizindikiro pa mphumi kapena pa dzanja, 10 nayenso adzamwa vinyo
waukali wa Mulungu, umene wathiridwa popanda kuchepetsa mphamvu
zake m'chikho cha ukali wa Mulungu. Munthuyo adzazunzidwa ndi
moto wamiyala yasulufure pamaso pa angelo oyera ndi pa Mwana
Wankhosa. 11 Ndipo utsi wa moto wowazunzawo udzakwera kumwamba
mpaka muyaya. Sikudzakhala kupumula usana ndi usiku kwa amene
anapembedza chirombo chija ndi fano lake kapena kwa aliyense amene
analembedwa chizindikiro cha dzina lake lija." 12 Pamenepa ndi pofunika
kupirira kwa anthu oyera mtima amene amasunga malamulo a Mulungu
ndi kukhalabe okhulupirika kwa Yesu.

13 Kenaka ndinamva mawu kuchokera kumwamba akuti, “Lemba kuti,
Odala anthu amene akufa ali mwa Ambuye kuyambira tsopano mpaka
m’tsogolo.”
“Inde,” akutero Mzimu, “akapumule ntchito zawo zotopetsa pakuti
ntchito zawo zidzawatsata.”

### *Zokolola za Dziko la Pansi*

14 Ndinayang’ana patsogolo panga ndinaona mtambo woyera patakha-
lapo wina ngati Mwana wa Munthu, kumutu atavala chipewa chau-
fumu chagolide ndipo m’dzanja mwake munali chikwakwa chakunthwa.
15 Tsono mngelo wina anatuluka m’Nyumba ya Mulungu nafuwula
mwamphamvu kwa uja wokhala pa mtamboyu. Mngeloyo anati, “Tenga
chikwakwa chako ndipo kolola, pakuti nthawi yokolola ya dziko la pansi
yakwana” 16 Choncho wokhala pa mtambo uja anayamba kukolola dzinthu
pa dziko lapansi ndi chikwakwa chakecho.
17 Mngelo wina anatuluka m’Nyumba ya Mulungu kumwamba ndipo
nayenso anali ndi chikwakwa chakunthwa. 18 Kenaka mngelo winanso
amene amalamulira moto, anatuluka kuchokera ku guwa lansembe nayi-
tana mwamphamvu mngelo uja amene anali ndi chikwakwa chakunthwa
chija, nati, “Tenga chikwakwa chako chakunthwacho yamba kudula
mphesa za m’munda wamphesa wa pa dziko lapansi, pakuti mphesa zapsa
kale.” 19 Pamenepo mngeloyo anayambadi kugwiritsa ntchito chikwakwa
chake nadula mphesa za dziko lapansi, naziponya m’chopondera mphesa
chachikulu cha ukali woopsa wa Mulungu. 20 Mphesazo zinapondedwa
m’chopondera mphesa kunja kwa mzinda. M’chopondera mphesamo
munatuluka magazi amene anayenderera ngati mtsinje, kuzama kwake
mita ndi theka ndipo kutalika kwake makilomita 300.

## 15

### *Angelo Asanu ndi Awiri Okhala ndi Miliri Isanu ndi Iwiri*

1 Kumwamba ndinaona chizindikiro china chachikulu ndi chodabwitsa:
angelo asanu ndi awiri ali ndi miliri isanu ndi iwiri yomaliza chifukwa Mu-
lungu anakwiya kotheratu. 2 Ndipo ndinaona chimene chinaoneka ngati
nyanja yonyezimira yosakaniza ndi moto, ndipo pambali pa nyanjayo
panayima amene anagonjetsa chirombo chija ndi fano lake, ndi nambala
yotanthauza dzina lake. Anthuwo ananyamula azeze amene Mulungu
anawapatsa. 3 Iwo ankayimba nyimbo ya Mose, mtumiki wa Mulungu,
ndi nyimbo ya Mwana Wankhosa. Nyimbo yake inkati,
“Zochita zanu ndi zazikulu ndi zodabwitsa,
    Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse
Njira zanu ndi zachilungamo ndi zoona,
    Mfumu ya mitundu yonse.
4 Inu Ambuye, ndani angapande kukuopani,
    ndi kulemekeza dzina lanu?
Pakuti Inu nokha ndiye woyera.
Anthu a mitundu yonse adzabwera
    kudzapembedza pamaso panu,
pakuti ntchito zanu zolungama zaonekera poyera.”
5 Zitatha izi, ndinaona kumwamba Nyumba ya Mulungu imene ndi
Tenti ya Umboni, atatsekula. 6 M’nyumbamo munatuluka angelo asanu
ndi awiri ndi miliri isanu ndi iwiri. Angelowo anavala nsalu zoyera
bwino zonyezimira ndi malamba agolide pa zifuwa zawo. 7 Ndipo kenaka

chimodzi cha zamoyo zinayi zija chinapereka kwa angelo asanu ndi awiri
mbale zisanu ndi ziwiri zodzaza ndi ukali wa Mulungu amene ali ndi moyo
mpaka muyaya. 8 Ndipo Nyumba ya Mulungu inadzaza ndi utsi wochokera
ku ulemerero wa Mulungu ndi ku mphamvu zake, ndipo panalibe yemwe
akanalowa m'Nyumbayo mpaka miliri isanu ndi iwiri ya angelo asanu ndi
awiri aja itatha.

# 16

*Mbale Zisanu ndi Ziwiri za Mkwiyo wa Mulungu*

1 Kenaka ndinamva mawu ofuwula kuchokera ku Nyumba ya Mulungu
ija kuwuza angelo asanu ndi awiri kuti, "Pitani, katsanulireni pa dziko
lapansi ukali wa Mulungu umene uli m'mbale zisanu ndi ziwirizi!"

2 Mngelo woyamba anapita natsanula mbale yake pa dziko lapansi
ndipo zilonda zoyipa ndi zowawa zinabuka pa anthu amene anali ndi
chizindikiro cha chirombo chija, napembedza fano lake.

3 Mngelo wachiwiri anapita natsanula mbale yake pa nyanja ndipo
madzi ake anasanduka magazi, magazi ake ngati a munthu wakufa.
Chamoyo chilichonse cha m'nyanjamo chinafa.

4 Mngelo wachitatu anapita natsanula mbale yake pa mitsinje ndi
akasupe amadzi ndipo zinasanduka magazi. 5 Kenaka ndinamva mngelo
wolamulira madzi uja akuti,

"Inu mwachita chilungamo, Inu Woyerayo,
amene mulipo ndipo munalipo;
6 pakuti iwo anakhetsa magazi a oyera anu ndi aneneri anu,
n'chifukwa chake mwawapatsa magazi kuti amwe, zomwe
zikuwayenera."

7 Kenaka ndinamva mawu ochokera ku guwa lansembe akuti,

"Inde, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse,
chiweruzo chanu ndi choona ndi cholungama."

8 Mngelo wachinayi anapita natsanula mbale yake pa dzuwa ndipo
dzuwa linapatsidwa mphamvu yopsereza anthu ndi moto. 9 Anapserera
nako kutentha kwakukuluko ndipo anatukwana Mulungu, amene anali
ndi ulamuliro pa miliri imeneyi, koma anakana kulapa ndi kumule-
mekeza.

10 Mngelo wachisanu anapita natsanula mbale yake pa mpando wau-
fumu wa chirombo chija ndipo mdima unagwa ponse pamene panali
ufumu wake. Anthu analuma malilime awo chifukwa cha ululu. 11 Ndipo
anatukwana Mulungu wakumwamba chifukwa cha maululu awo ndi
zilonda zawo koma anakana kulapa pa zimene anachita.

12 Mngelo wachisanu ndi chimodzi anapita natsanula mbale yake pa
mtsinje waukulu wa Yufurate, ndipo madzi ake anaphwa kuti pakhale
njira yodzera mafumu ochokera kummawa. 13 Kenaka ndinaona mizimu
yoyipa itatu imene inkaoneka ngati achule; inatuluka m'kamwa mwa
chinjoka chija, m'kamwa mwa chirombo chija ndi m'kamwa mwa
mneneri wonyenga uja. 14 Imeneyi ndiyo mizimu ya ziwanda imene
imachita zizindikiro zodabwitsa ndipo imatuluka kupita kwa mafumu
a dziko lonse, kukawasonkhanitsa ku nkhondo ya pa tsiku lalikulu la
Mulungu Wamphamvuzonse.

15 “Taonani, ndikubwera ngati mbala! Wodala munthu amene ali
maso, nasunga zovala zake, kuti asayende maliseche kuti angaonetse
maliseche ake.”

16 Kenaka mizimu ija inasonkhanitsa pamodzi mafumu ku malo amene
m’Chihebri amatchedwa Armagedo.

17 Mngelo wachisanu ndi chiwiri anatsanulira mbale yake mu mlen-
galenga ndipo ku Nyumba ya Mulungu kunamveka mawu ofuwula
kuchokera ku mpando waufumu kuti, “Kwatha!” 18 Kenaka kunachitika
mphenzi, phokoso, mabingu ndi chivomerezi choopsa. Chivomerezi
ngati ichi sichinachitikepo chikhalire cha munthu pa dziko lapansi.
Chinali chivomerezi choopsa kwambiri. 19 Mzinda waukuluwo unagawika
magawo atatu ndipo mizinda ya mitundu ya anthu inagwa. Mulungu
anakumbukira Babuloni Wamkulu namupatsa chikho chake chodzaza ndi
vinyo wa ukali wa mkwiyo wake. 20 Chilumba chilichonse chinathawa
ndipo mapiri sanaonekenso. 21 Matalala akuluakulu olemera pafupifupi
makilogalamu makumi asanu anagwa kuchokera kumwamba kugwera pa
anthu. Ndipo anthu anatukwana Mulungu chifukwa cha mliri wa matalala
popeza unali mliri woopsa kwambiri.

# 17

### *Mkazi Wachiwerewere*

1 Mmodzi wa angelo asanu ndi awiri aja amene anali ndi mbale
zisanu ndi ziwiri anadza nati kwa ine, “Bwera ndikuonetse chilango cha
mkazi wadama wotchuka uja amene akukhala pambali pa madzi ambiri.
2 Mafumu a dziko lapansi amachita naye chigololo ndipo okhala pa dziko
lapansi analedzera ndi vinyo wa zigololo zake.”

3 Kenaka mngeloyo anandinyamula mwa Mzimu Woyera kupita nane
ku chipululu. Kumeneko ndinaona mkazi atakhala pa chirombo chofiira
chokutidwa ndi mayina a chipongwe ndipo chinali ndi mitu isanu ndi
iwiri ndi nyanga khumi. 4 Mkaziyo anavala zovala za pepo ndi zofiira
nadzikongoletsa ndi golide, miyala yapamwamba ndi ngale. Ananyamula
chikho chagolide m’dzanja lake, chodzaza ndi zinthu zonyansa ndi
fungo loyipa la zigololo zake. 5 Pa mphumi pake panalembedwa dzina
lodabwitsa:

BABULONI WAMKULU
MAYI WA AKAZI ADAMA
NDI WAZOYIPITSA ZA DZIKO LAPANSI.

6 Ndinaona kuti mkaziyo anali ataledzera ndi magazi a oyera mtima,
magazi a amene anachitira umboni Yesu.

Nditamuona mkaziyo ndinadabwa kwambiri. 7 Kenaka mngelo uja anati
kwa ine, “Bwanji ukudabwa? Ndikufotokozera chinsinsi cha mkaziyu ndi
chinsinsi cha chirombo chimene wakwerapochi chokhala ndi mitu isanu
ndi iwiri ndi nyanga khumi. 8 Chirombo chimene wachionachi chinalipo
kale koma tsopano kulibe ndipo chidzatuluka ku chidzenje chakuya ndi
kupita kukawonongedwa. Anthu okhala pa dziko lapansi amene mayina
awo sanalembedwe m’buku lamoyo kuyambira pa kulengedwa kwa dziko
lapansi adzadabwa pamene adzaona chirombocho, chifukwa chinalipo
kale, tsopano kulibe, komabe chidzabwera.

9 “Zimenezi zikufunika kuganizira mwanzeru. Mitu isanu ndi iwiriyo
ndi mapiri asanu ndi awiri pomwe mkazi uja amakhalirapo. Yomweyonso
ndi mafumu asanu ndi awiri. 10 Mafumu asanu anagwa, imodzi ilipo ndipo
ina sinabwere; koma pamene idzafika, idzayenera kukhala kwa kanthawi
kochepa. 11 Chirombo chomwe chinalipo kale ndipo tsopano kulibe ndiyo
mfumu yachisanu ndi chitatu. Iyo ndi ya m’gulu la asanu ndi awiriwo
ndipo ikupita kukawonongedwa.

12 “Nyanga khumi unaziona zija ndi mafumu khumi amene sanapat-
sidwe ulamuliro, koma adzapatsidwa ulamuliro pamodzi ndi chirombo
kwa ora limodzi. 13 Mafumuwo ali ndi cholinga chimodzi ndipo
adzapereka mphamvu ndi ulamuliro wawo kwa chirombocho. 14 Iwo
adzachita nkhondo ndi Mwana Wankhosa, koma Mwana Wankhosayo
adzawagonjetsa chifukwa Iye ndi Mbuye wa ambuye ndi Mfumu ya
mafumu, ndipo amene adzakhala ndi Iye ndi oyitanidwa ake, osankhidwa
ndi otsatira ake okhulupirika.”

15 Kenaka mngeloyo anati kwa ine, “Madzi amene unawaona pamene
mkazi wadamayo anakhalapo ndiwo anthu ochuluka, mitundu ndi
ziyankhulo. 16 Nyanga khumi ndi chirombo unazionazo zidzadya mkazi
wadamayo. Zidzamufwifwitsa ndi kumusiya wamaliseche; zidzadya
nyama yake ndi kumutentha ndi moto. 17 Pakuti Mulungu wayika
ichi m’mitima mwawo kuti akwaniritse cholinga chake povomerezana
kupereka mphamvu zawo zolamulira kwa chirombo, kufikira Mawu a
Mulungu atakwaniritsidwa. 18 Mkazi unamuonayo ndi mzinda waukulu
umene ulamulira mafumu a dziko lapansi.”

# 18

### *Kugwa kwa Babuloni*

1 Zitatha izi ndinaona mngelo wina akutsika kuchokera kumwamba. Iye
anali ndi ulamuliro waukulu, ndipo dziko lapansi linawala ndi ulemerero.
2 Mngeloyo anafuwula ndi mawu amphamvu kuti:
“ ‘Wagwa! Wagwa Babuloni Wamkulu!’
Wasandulika mokhalamo ziwanda
ndi kofikako mizimu yonse yoyipa
ndi mbalame zonse zonyansa
ndi zodetsedwa.
3 Pakuti mayiko onse amwa
vinyo ozunguza mutu wazigololo zake.
Mafumu a dziko lapansi achita naye chigololo,
ndipo amalonda a dziko lapansi analemera kuchokera pa zolakalaka
zake zosefukira.”

### *Awachenjeza kuti Athawe Chiweruzo cha Babuloni*

4 Ndiponso ndinamva mawu ena kuchokera kumwamba akuti:
“ ‘Anthu anga tulukani, mwa iye,’
mungachimwe naye
kuti musadzalandire nawo gawo lililonse la miliri yake;
5 pakuti machimo ake awunjikana mpaka kumwamba,
ndipo Mulungu wakumbukira milandu yake.
6 Bwezerani Iye monga momwe iye anakuchitirani.
Mubwezereni mowirikiza pa zimene anachita.
Mumusakanizire magawo awiri kuchokera m’chikho chake.

7 Mumuzunze, kumumvetsa chisoni kwambiri
monga mwaulemerero ndi zolakalaka
zimene anadzaza mu mtima mwake. Iye anadzikuza n'kumati,
'Ndinakhala monga mfumu yayikazi,
ine sindine wamasiye
ndipo sindidzalira maliro.'
8 Chifukwa chake miliri yake idzamugonjetsa tsiku limodzi;
imfa, kulira maliro ndi njala.
Iye adzanyeka ndi moto
pakuti wamphamvu ndi Mulungu Ambuye amene wamuweruza.

*Tsoka la Babuloni*

9 "Mafumu a dziko lapansi, amene anachita naye chigololo nachita naye
pamodzi zosangalatsa moyo uno, akadzaona utsi wa kunyeka kwake,
adzalira nakhuza maliro ake. 10 Iwo adzayima kutali nalira chifukwa
choopsedwa ndi mazunzo ake.
" 'Tsoka! Tsoka mzinda waukulu
iwe, Babuloni mzinda wamphamvu!
Mu ora limodzi chiwonongeko chako chafika!'
11 "Amalonda a dziko lapansi adzalira nakhuza maliro ake chifukwa pal-
ibenso amene akugula katundu wawo, 12 katundu wagolide, siliva, miyala
yamtengo wapamwamba ndi ngale; nsalu zoyera kwambiri zapamwamba
ndi zofiira; nsalu zasilika ndi zapepo; mitengo iliyonse yonunkhira ndi
zinthu zilizonse zopangidwa ndi mnyanga, kapena matabwa ogulidwa ndi
ndalama zambiri kapena mkuwa kapena chitsulo ndi mwala wonyezimira;
13 zokometsera zakudya, mure, lubani ndi zofukiza zina, vinyo ndi mafuta
a olivi, ufa wosalala ndi tirigu; ng'ombe ndi nkhosa; akavalo ndi ngolo;
ndi anthu adzagulitsidwa ukapolo.
14 "Iwo adzanena kuti, 'Chipatso chimene unachilakalaka chakuchok-
era. Chuma chako chonse ndi ulemerero zatha, sizidzapezekanso.'
15 Amalonda amene anagulitsa zinthu izi napeza chuma kuchokera kwa
iye adzayima patali potero ataopsedwa ndi mazunzo ake. Adzalira ndi
kukhuza maliro 16 ndipo adzalira mokuwa kuti,
" 'Tsoka! Tsoka! Mzinda waukulu,
iwe wovala nsalu zoyera kwambiri, zapepo ndi zofiira,
ndi wonyezimira ndi golide, miyala yamtengo wapamwamba ndi
ngale!
17 Chuma chambiri choterechi chafika powonongeka mu ora limodzi!'
"Oyendetsa sitima ndi onse oyenda pa sitima ya pamadzi, ogwira
ntchito m'sitima ndi onse amene amadalira nyanja pamoyo wa tsiku
ndi tsiku adzayima patali potero. 18 Akadzaona utsi wa kunyeka kwake,
adzakuwa kuti, 'Kodi panalinso mzinda wina ngati mzinda waukuluwu?'
19 Adzathira fumbi pamitu pawo ndipo adzalira nakhuza maliro kuti,
"Tsoka! Tsoka mzinda waukulu iwe,
kumene onse anali ndi sitima pa nyanja
analemera kudzera m'chuma chake!
Mu ora limodzi wawonongedwa.

20 "Kondwerani chifukwa cha iye inu kumwamba!
Kondwerani oyera mtima
ndi atumwi ndi aneneri!
Mulungu wamuweruza iye
monga momwe anakuchitirani inu."

*Chiwonongeko Chotsiriza cha Babuloni*

21 Kenaka mngelo wamphamvu ananyamula mwala waukulu ngati mphero yayikulu nawuponya m'nyanja nanena kuti,
“Mwa mphamvu chonchi
mzinda waukulu wa Babuloni udzaponyedwa pansi,
sudzapezekanso.
22 Mwa iwe simudzamvekanso liwu la woyimba zeze, ndi akatswiri a zoyimbayimba,
oyimba zitoliro, ndi lipenga.
Mwa iwe simudzapezekanso
m'misiri wina aliyense.
Mwa iwe simudzapezekanso
phokoso la mphero.
23 Kuwala kwa nyale
sikudzawunikanso mwa inu.
Mawu a mkwati ndi mkwatibwi
sadzamvekanso mwa iwe.
Amalonda anu anali akuluakulu a dziko lapansi.
Mitundu yonse inasokonezedwa ndi zamatsenga zako.
24 Mwa iye munapezeka magazi a aneneri ndi a oyera mtima,
ndi onse amene anaphedwa pa dziko lapansi.”

# 19

*Babuloni Wagwa, Haleluya!*

1 Zitatha izi, ndinamva chimene chinamveka ngati phokoso la gulu lalikulu mmwamba likufuwula kuti,
“Haleluya!
Chipulumutso ndi ulemerero ndi mphamvu ndi za Mulungu wathu,
2 pakuti chiweruzo chake ndi choona ndi cha chilungamo.
Iye waweruza mkazi wadama wotchuka uja
amene anayipitsa dziko lonse lapansi ndi zigololo zake.
Iye wabwezera pa mkaziyo magazi a atumiki ake.”
3 Ndipo anafuwulanso kuti,
“Haleluya!
Utsi wochokera kwa mkazi wadamayo udzakwera kumwamba mpaka muyaya.”
4 Akuluakulu 24 aja ndi zamoyo zinayi zija anadzigwetsa pansi kupembedza Mulungu amene anakhala pa mpando waufumu. Ndipo anafuwula kuti,
“Ameni, Haleluya!”
5 Kenaka mawu anachoka ku mpando waufumu kuti,
“Lemekezani Mulungu wathu
inu nonse atumiki ake,
inu amene mumamuopa,
nonse ang'ono ndi akulu!”
6 Kenaka ndinamva chimene chinamveka ngati gulu lalikulu, ngati mkokomo wamadzi othamanga ndipo ngati kugunda kwakukulu kwa bingu, ndipo anati,
“Haleluya!
Pakuti Ambuye Mulungu wathu Wamphamvuzonse akulamulira.
7 Tiyeni tisangalale ndi kukondwera
ndi kumutamanda!

Pakuti nthawi ya ukwati wa Mwana Wankhosa yafika,
ndipo Mkwatibwi wakonzekeratu.
8 Wapatsidwa nsalu yoyera kwambiri, yowala ndi yosada
kuti avale."
(Nsalu yoyera kwambiri ikuyimira ntchito zolungama za oyera mtima).
9 Kenaka mngelo anandiwuza kuti, "Lemba kuti, Odala amene ayi-
tanidwa ku phwando la ukwati wa Mwana Wankhosa." Ndipo anatinso,
"Awa ndiwo mawu woona a Mulungu."
10 Pamenepo ndinadzigwetsa pa mapazi ake kumupembedza. Koma
anandiwuza kuti, "Usatero ayi, ine ndine mtumiki mnzako ngati iwe
yemwe, ndiponso ngati abale ako amene asunga umboni wa Yesu.
Pembedza Mulungu. Pakuti umboni wa Yesu ndiye mzimu wa uneneri."

### *Wokwera pa Kavalo Woyera*

11 Ndinaona kumwamba kutatsekuka ndipo patsogolo panga panali
kavalo woyera, amene anakwerapo dzina lake linali Wokhulupirika
ndiponso Woona. Poweruza ndi kuchita nkhondo, amachita molungama.
12 Maso ake anali ngati malawi amoto, ndipo pamutu pake panali zipewa
zaufumu zambiri. Anali ndi dzina lolembedwa, lodziwika ndi Iye yekha,
osati wina aliyense. 13 Iye anavala mkanjo woviyika m'magazi, ndipo
dzina lake ndi Mawu a Mulungu. 14 Magulu ankhondo akumwamba
ankamutsatira atakwera pa akavalo oyera, ndipo iwowo atavala nsalu
zoyera kwambiri ndi zosada. 15 M'kamwa mwake munatuluka lupanga
lakuthwa limene anati akaphe nalo mitundu ya anthu. Iye adzalamulira
ndi ndodo yachitsulo. Iye anaponda choponderamo mphesa cha ukali
wa Mulungu Wamphamvuzonse. 16 Pa chovala ndi pa ntchafu pake
panalembedwa dzina ili:

MFUMU YA MAFUMU NDI MBUYE WA AMBUYE.

17 Ndipo ndinaona mngelo atayimirira pa dzuwa amene anafuwula ndi
mawu okweza kwa mbalame zonse zowuluka mlengalenga kuti, "Bwerani,
sonkhanani pamodzi ku phwando lalikulu la Mulungu. 18 Kuti mudye
mnofu wa mafumu, wa akulu a ankhondo, ndi wa anthu amphamvu,
wa akavalo ndi okwerapo awo, ndi wa anthu onse, mfulu ndi akapolo,
ang'ono ndi aakulu."
19 Kenaka ndinaona chirombo chija ndi mafumu a dziko lapansi
ndi magulu ankhondo atasonkhana pamodzi kuti achite nkhondo ndi
wokwera pa kavalo ndi ankhondo ake. 20 Koma chirombocho chinag-
widwa pamodzi ndi mneneri wonyenga uja amene anachita zizindikiro
zodabwitsa pamaso pake. Ndi zizindikirozi anasocheretsa amene analem-
bedwa chizindikiro cha chirombocho napembedza fano lake. Onse awiri
anaponyedwa amoyo m'nyanja yamoto yasulufule wotentha. 21 Ena onse
anaphedwa ndi lupanga lija linatuluka m'kamwa mwa wokwera pa kavalo
uja, ndipo mbalame zonse zinadya mokwanira mnofu wa anthu akufawo.

## 20

### *Zaka 1,000*

1 Ndipo ndinaona mngelo akutsika kuchokera kumwamba ali ndi
kiyi ya ku chidzenje chakuya chija atanyamula m'dzanja lake unyolo
waukulu. 2 Iye anachigwira chinjokacho, chinjoka chakalekale chija,
amene ndi Mdierekezi kapena kuti Satana, ndipo anamumanga zaka
1,000. 3 Anamuponya ku chidzenje chakuya chija namutsekera ndi kiyi
ndi kumatirira pa khomopo kuti asatulukenso kukanyenga mitundu ya

anthu mpaka patapita zaka 1,000. Zikadzatha zakazo, adzamumasula kwa kanthawi pang'ono chabe.
4 Ndinaona mipando yaufumu pamene anakhalapo anthu amene anapatsidwa mphamvu zoweruza. Ndipo ndinaona mizimu ya amene anadulidwa makosi chifukwa cha umboni wa Yesu ndi chifukwa cha Mawu a Mulungu. Iwo sanapembedze nawo chirombo kapena fano lake ndipo sanalembedwe chizindikiro chake pa mphumi zawo kapena pa manja awo. Iwo anakhalanso ndi moyo nalamulira pamodzi ndi Khristu zaka 1,000. 5 (Akufa ena onse sanaukenso mpaka zitatha zaka
1,000). Uku ndiko kuuka kwa akufa koyamba. 6 Odala ndi oyera mtima
amene adzaukitsidwa nawo pa kuukitsidwa koyamba. Imfa yachiwiri ilibe mphamvu pa iwo koma adzakhala ansembe a Mulungu ndi a Khristu ndipo adzalamulira naye pamodzi zaka 1,000.

### *Kugonjetsedwa kwa Satana*

7 Zaka 1,000 zikadzatha, Satana adzamasulidwa ku ndende yake 8 ndipo
adzapita kukanyenga mitundu ya anthu kumbali zonse zinayi za dziko lapansi, Gogi ndi Magogi, kuwasonkhanitsa kuti akachite nkhondo. Kuchuluka kwawo kudzakhala ngati mchenga wa m'mbali mwa nyanja.
9 Iwo anayenda ponseponse pa dziko lapansi nazinga msasa wa anthu a Mulungu, mzinda umene Iye amawukonda. Koma moto unatsika
kuchokera kumwamba ndi kuwanyeketsa. 10 Ndipo Mdierekezi amene
anawanyenga, anaponyedwa m'nyanja ya sulufule wotentha, kumene kunaponyedwa chirombo chija ndi mneneri wonama uja. Iwo adzazunzika usiku ndi usana kwamuyaya.

### *Chiweruzo Chotsiriza*

11 Kenaka ndinaona Mpando Waufumu waukulu woyera ndi Iye amene
anakhalapo. Dziko lapansi ndi kumwamba zinathawa pamaso pake ndipo
panalibenso malo awo. 12 Ndipo ndinaona akufa, aakulu ndi aang'ono
omwe atayimirira patsogolo pa Mpando Waufumu ndipo mabuku anatsekulidwa. Buku lina linatsekulidwa limene linali Buku Lamoyo. Akufa anaweruzidwa monga mwa zimene anachita monga mmene zinalembedwera m'mabuku. 13 Nyanja inapereka amene anaferamo ndipo imfa ndi
Hade zinapereka akufa ake ndipo munthu aliyense anaweruzidwa monga
mwa ntchito zake. 14 Kenaka imfa ndi Hade zinaponyedwa m'nyanja ya
moto. Nyanja yamoto ndiyo imfa yachiwiri. 15 Ngati dzina la wina aliyense
silinapezeke m'Buku Lamoyo, anaponyedwa m'nyanja yamoto.

## 21

### *Kumwamba ndi Dziko Lapansi Zatsopano*

1 Kenaka ndinaona kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano pakuti kumwamba koyamba ndi dziko lapansi loyamba zinapita
ndipo kunalibenso nyanja ina iliyonse. 2 Ndinaona mzinda wopatulika,
Yerusalemu watsopano, ukutsika kuchokera kumwamba kwa Mulungu, utakonzedwa ngati mkwatibwi wovala zokongola kukonzekera mwamuna
wake. 3 Ndipo ndinamva mawu ofuwula kuchokera ku Mpando Waufumu
kuti, "Taonani! Malo wokhalapo Mulungu ali pakati pa anthu, ndipo Iye adzakhala ndi anthuwo. Iwo adzakhala anthu ake ndipo Mulungu mwini
adzakhala nawo nakhala Mulungu wawo. 4 'Mulungu adzapukuta misozi
yonse m'maso mwawo. Sikudzakhalanso imfa kapena kukhuza maliro kapena kulira kapena ululu popeza zakale zapita.' "

5 Amene anakhala pa mpando waufumuyo anati, “Ndikulenga zinthu
zonse zikhale zatsopano!” Ndipo anati, “Lemba izi, pakuti mawu awa ndi
okhulupirika ndi woona.”

6 Iye anandiwuza kuti, “Kwatha. Ine ndine Alefa ndi Omega, Woyamba
ndi Wotsiriza. Kwa onse akumva ludzu, ndidzawapatsa zakumwa zaulere
zochokera ku kasupe wamadzi amoyo. 7 Iye amene adzapambane
adzalandira zonsezi, ndipo ndidzakhala Mulungu wake ndi Iye adzakhala
mwana wanga. 8 Koma amantha, osakhulupirira, okonda zonyansa,
opha anthu, achiwerewere, amatsenga, opembedza mafano ndi abodza,
malo awo adzakhala nyanja yamoto ya sulufule wotentha. Iyi ndi imfa
yachiwiri.”

### *Mzinda wa Yerusalemu Watsopano*

9 Mmodzi wa angelo asanu ndi awiri aja, anali ndi mbale zisanu
ndi ziwiri zodzaza ndi miliri yotsiriza isanu ndi iwiri anandiwuza kuti,
“Bwera, ine ndidzakuonetsa mkwatibwi wa Mwana Wankhosa.” 10 Ndipo
anandinyamula mwa Mzimu Woyera kupita nane ku phiri lalikulu ndi
lalitali nandionetsa mzinda wopatulika, Yerusalemu ukutsika kuchokera
kumwamba kwa Mulungu. 11 Unawala ndi ulemerero wa Mulungu, ndipo
kuthwanima kwake kunali ngati mwala wamtengowapatali, ngati jasipa;
woyera ngati krustalo. 12 Mzindawo unali ndi mpanda waukulu ndi
wautali, unali ndi zipata khumi ndi ziwiri, ndipo panali angelo khumi ndi
awiri. Pa chipata chilichonse panayima mngelo. Pa chipata chilichonse
panalembedwa dzina la fuko la Israeli. 13 Kummawa kunali zipata zitatu,
kumpoto zitatu, kummwera zitatu ndi kumadzulo zitatu. 14 Mpanda wa
mzindawu unali ndi maziko khumi ndi awiri ndipo pa mazikopo panali
mayina khumi ndi awiri a atumwi a Mwana Wankhosa.

15 Mngelo amene ankayankhula nane uja anali ndi ndodo yagolide
yoyezera mzindawo, zipata zake ndi mpanda wake. 16 Mzindawo
unamangidwa mofanana kutalika kwake, mulitali ndi mulifupi munali
mofanana. Anayeza mzindawo ndi ndodo ija ndipo anapeza kuti mulitali,
mulifupi ndi msinkhu wake kutalika kwake kunali makilomita 2,200.
17 Anayesa mpanda uja ndipo kuchindikala kwake kunali kopitirirapo
mamita 65 monga mwa muyeso wa anthu umene mngelo anagwiritsa
ntchito. 18 Mpandawo unapangidwa ndi yasipa, ndipo mzindawo unali
wagolide oyengeka owala ngati galasi. 19 Maziko a mpanda wa mzindawo
anali okongoletsedwa ndi miyala yamtengowapatali ya mtundu uliwonse.
Maziko oyamba anali yasipa, achiwiri anali safiro, achitatu ndi kalikedo,
achinayi ndi simaragido, 20 achisanu ndi sardiyo, achisanu ndi chiwiri
ndi krusolito, achisanu ndi chitatu ndi berulo, achisanu ndi chinayi ndi
topaziyo, a khumi ndi krusoprazo, a khumi ndi chimodzi ndi huakito,
a khumi ndi chiwiri ndi emetusto. 21 Zipata khumi ndi ziwiri zija
zinapangidwa ndi ngale, chipata chilichonse chinapangidwa ndi ngale
imodzi. Misewu ya mzindawo inali yopangidwa ndi golide oyengeka,
owala ngati galasi.

22 Ine sindinaone Nyumba ya Mulungu iliyonse mu mzindawo chi-
fukwa Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse ndi Mwana Wankhosa ndiwo
Nyumba yake. 23 Palibe chifukwa choti dzuwa kapena mwezi ziwale
popeza mu mzindawo ulemerero wa Mulungu ndiwo umawalamo ndipo
nyale yake ndi Mwana Wankhosa uja. 24 Mitundu ya anthu idzayenda
m’kuwala kwake ndipo mafumu a dziko lapansi adzabweretsa ulemerero

wawo mu mzindamo. 25 Zipata zake sizidzatsekedwa ngakhale tsiku
limodzi lomwe pakuti sikudzakhala usiku kumeneko. 26 Ulemerero
ndi ulemu wa mitundu ya anthu adzapita nazo kumeneko. 27 Kanthu
kosayeretsedwa sikadzalowamo, kuphatikizanso aliyense wochita zinthu zochititsa manyazi ndi zachinyengo, koma okhawo amene mayina awo alembedwa m'buku lamoyo la Mwana Wankhosa.

# 22

*Mtsinje Wamoyo*

1 Ndipo mngeloyo anandionetsa mtsinje wamadzi amoyo, oyera ngati mwala wa krustalo ukutuluka ku mpando waufumu wa Mulungu ndi
wa Mwana Wankhosa, 2 Ukuyenda pakati pa msewu waukulu wa mu mzindawo. Mbali iliyonse ya mtsinjewo kunali mtengo wamoyo, utabala zipatso khumi ndi ziwiri. Kubereka zipatso mwezi uliwonse. Ndipo masamba a mtengowo ndi mankhwala wochiritsa anthu a mitundu ina.
3 Sipadzakhalanso temberero lililonse. Mpando waufumu wa Mulungu ndi wa Mwana Wankhosa udzakhala mu mzindawo, ndipo atumiki
ake adzamutumikira. 4 Iwo adzaona nkhope yake ndipo dzina lake
lidzalembedwa pa mphumi zawo. 5 Sipadzakhalanso usiku. Sadzafuna kuwala kwa nyale kapena kwa dzuwa pakuti Ambuye Mulungu adzakhala kuwala kwawo. Ndipo adzalamulira kwamuyaya.

6 Mngeloyo anandiwuza kuti, "Mawu awa ndi okhulupirika ndi owona. Ambuye Mulungu wa mizimu ya aneneri anatumiza mngelo wake kudza-onetsa atumiki ake zinthu zimene ziyenera kuchitika posachedwapa."

*Yesu Akubweranso*

7 "Taonani, ndikubwera posachedwa! Wodala ndi amene asunga mawu oneneratu za kutsogolo a m'buku ili."

8 Ine Yohane, ndine amene ndinamva ndi kuona zinthu izi. Ndipo pamene ndinamva ndi kuona izi ndinagwa pansi kuti ndipembedze
mngelo amene amandionetsa zimenezi. 9 Koma mngeloyo anandiwuza
kuti, "Usatero ayi! Ine ndine wotumikira monga iwe pamodzi ndi abale ako aneneri ndi onse amene amasunga mawu a m'buku pembedzani Mulungu."

10 Kenaka anandiwuza kuti, "Usabise mawu onena zam'tsogolo a
m'buku ili chifukwa nthawi yayandikira. 11 Wochita zoyipa apitirire
kuchita zoyipazo; wochita zonyansa apitirire kuchita zonyansazo; wochita zabwino apitirire kuchita zabwinozo; ndipo woyera mtima apitirire kukhala woyera mtima."

*Mawu Otsiriza: Kuyitanidwa ndi Chenjezo*

12 "Taonani, ndikubwera posachedwa! Ndikubwera ndi mphotho zanga
kuti ndidzapereke kwa aliyense malinga ndi zimene anachita. 13 Ine
ndine Alefa ndi Omega, Woyamba ndi Wotsiriza, Chiyambi ndi Chimaliziro ndine.

14 "Odala amene achapa mikanjo yawo, kuti akhale ndi ufulu wopita ku
mtengo wamoyo ndi kuti akalowe m'zipata za mu mzindawo. 15 Kunja
kuli agalu, amatsenga, achiwerewere, akupha anthu, opembedza mafano ndi aliyense amene amakonda bodza ndi kulichita.

16 "Ine Yesu, ndatuma mngelo wanga kuti achitire umboni uwu ku mipingo. Ine ndine Muzu ndi Chipatso cha Davide ndipo ndine Nthanda Yonyezimira."

17 Mzimu Woyera ndi mkwatibwi akuti, “Bwerani!” Ndipo amene
akumva anena kuti Bwerani! Iye amene ali ndi ludzu abwere, ndipo
aliyense amene afuna alandire mphatso yaulere ya madzi amoyo.

18 Ndikuchenjeza aliyense amene akumva mawu onena zam’tsogolo a
m’bukuli kuti, “Ngati wina awonjezerapo kalikonse, Mulungu adzamu-
wonjezera miliri imene yalembedwa m’buku ili.
19 Ndipo wina akachot-
sapo mawu onena zam’tsogolo a m’buku ili, Mulungu adzachotsa gawo
lake pa mtengo wamoyo ndi la mu mzinda woyera zimene zanenedwa
m’buku ili.”

20 Iye amene akuchitira umboni pa zinthu izi akuti, “Inde, Ine ndikub-
wera posachedwa.”

Ameni. Bwerani Ambuye Yesu.

21 Chisomo cha Ambuye Yesu chikhale ndi anthu onse. Ameni.